Malawi Old Testament 1992

©The Bible Society of Malawi, 1992

Genesis

Genesis 1

1PACIYAMBI Mulungu adalenga kumwamba ndi dziko lapansi. 2Dziko lapansi
ndipo linali lopanda kanthu; ndipo mdima unali pamwamba pa nyanja; ndipo
mzimu wa Mulungu unaliokufungatira pamwamba pa madzi. 3Ndipo anati
Mulungu, Kuyere; ndipo kunayera. 4Ndipo anaona Mulungu kuti kuyerako kunali
kwabino: ndipo Mulungu analekanitsa kuyera ndi mdima. 5Ndipo Mulungu
anacha kuyerako Usana, ndi mdimawo anaucha Usiku. Ndipo panali madzulo
ndipo panali m'mawa, tsiku loyamba.
6Ndipo anati Mulungu, Pakhale thambo pakati pa madzi, lilekanitse madzi ndi
madzi. 7Ndipo Mulungu anapanga thambo, nalekanitsa madzi anali pansi pa
thambolo ndi madzi analf pamwamba pa thambolo: ndipo kunatero. 8Ndipo
Mulungu analicha thambolo Kumwamba. Ndipo panali madzulo ndipo panali
m'mawa, tsiku laciwiri.
9Ndipo anati Mulungu, Madzi a pansi pa kumwamba asonkhane pamodzi pa
malo amodzi, uoneke mtunda: ndipo kunatero. 10Ndipo Mulungu adaucha
mtundawo Dziko lapansi; kusonkhana kwa madziko ndipo adaucha Nyanja:
ndipo anaona Mulungu kuti kunali kwabwino. 11Mulungu ndipo anati, Dziko
lapansi limere maudzu, therere lobala mbeu, ndi mtengo wazipatso wakubala
zipatso monga mwa mtundu wace, momwemo muli mbeu yace, pa dziko
lapansi: ndipo kunatero. 12Ndipo dziko lapansi linamera maudzu, therere lobala
mbeu monga mwa mtundu wace, ndi mtengo wakubala zipatso, momwemo
muli mbeu yace, monga mwa mtundu wace; ndipo anaona Mulungu kuti kunali
kwabwino. 13Ndipo panali madzulo ndipo panali m'mawa, tsiku lacitatu.
14Ndipo Mulungu anati, Pakhale zounikira pa thambo la kumwamba,
zakulekanitsa usana ndi usiku; zikhale zizindikiro ndi nyengo, ndi masiku, ndi
zaka; 15zikhale zounikira m'thambo la kumwamba, kuti ziunikire pa dziko
lapansi; ndipo kunatero. 16Ndipo Mulungu anapanga zounikira zazikuru ziwiri;
counikira cacikuru cakulamulira usana, counikira cacing'ono cakulamulira usiku,
ndi nyenyezi zomwe. 17Mulungu ndipo adaika zimenezo m'thambo la
kumwamba, kuti ziunikire pa dziko lapansi, 18nizilamulire usana ndi usiku,
nizilekanitse kuyera ndi mdima: ndipo anaona Mulungu kuti kunali
kwabino. 19Ndipo panali madzulo ndipo panali m'mawa, tsiku lacinai.
20Ndipo anati Mulungu, Madzi abale zocuruka zamoyo zoyendayenda, ndi
mbalame ziuluke pamwamba pa dziko lapansi ndi pamlengalenga. 21Mulungu
ndipo adalenga zinsomba zazikuru ndi zoyendayenda zamoyo zakucuruka
m'madzi mwa mitundu yao, ndi mbalame zamapiko, yonse monga mwa mtundu
wace: ndipo anaona Mulungu kuti kunali kwabwino. 22Mulungu ndipo
anadalitsa zimenezo, nati, Zibalane, zicuruke, zidzaze madzi a m'nyanja, ndi
mbalame zicuruke pa dziko lapansi. 23Ndipo panali madzulo ndipo panali
m'mawa, tsiku lacisanu.

24Ndipo adati Mulungu, Dziko lapansi libale zamoyo monga mwa mitundu yao, ng'ombe, ndi zokwawa, ndi zinyama za dziko lapansi monga mwa mitundu yao: ndipo kunatero. 25Ndipo Mulungu anapanga zinyama za dziko lapansi monga mwa mitundu yao; ndi ng'ombe monga mwa mtundu wace, ndi zonse zakukwawa pansi monga mwa mitundu yao; ndipo Mulungu anaona kuti kunali kwabwino.

Kulengedwa kwa munthu

26Ndipo anati Mulungu, Tipange munthu m'cifanizo cathu, monga mwa cikhalidwe cathu: alamulire pa nsomba za m'nyanja, ndi pa mbalame za m'mlengalenga, ndi pa ng'ombe, ndi pa dziko lonse lapansi, ndi pa zokwawa zonse zakukwawa pa dziko lapansi. 27Mulungu ndipo adalenga munthu m'cifanizo cace, m'cifanizo ca Mulungu adamlenga iye; adalenga iwo mwamuna ndi mkazi. 28Mulungu ndipo anadalitsa iwo, ndipo adati kwa iwo, Mubalane, mucuruke, mudzaze dziko lapansi, muligonjetse: mulamulire pa nsomba za m'nyanja, ndi pa mbalame za m'mlengalenga, ndi pa zamoyo zonse zakukwawa pa dziko lapansi. 29Ndipo anati Mulungu, Taonani, ndakupatsani inu therere lonse lakubala mbeu liri pa dziko lapansi, ndi mitengo yonse m'mene muli cipatso ca mtengo wakubala mbeu; cidzakhala cakudya ca inu: 30ndiponso ndapatsa zinyama zonse za dziko lapansi, ndi mbalame zonse za m'mlengalenga, ndi zakukwawa zonse za dziko lapansi m'mene muli moyo, therere laliwisi lonse likhale cakudya: ndipo kunatero. 31Ndipo anaziona Mulungu zonse zimene adazipanga, ndipo, taonani, zinali zabwino ndithu. Ndipo panali madzulo ndipo panali m'mawa, tsiku lacisanu ndi cimodzi.

Genesis 2

1Ndipo zinatha kupangidwa zakumwamba ndi dziko lapansi, ndi khamu lao
lonse. 2Tsiku lacisanu ndi ciwiri Mulungu anamariza nchito yonse anaipanga;
ndipo anapuma tsiku lacisanu ndi ciwiri ku nchito yace yonse. 3Mulungu ndipo
anadalitsa tsiku lacisanu ndi ciwiri, naliyeretsa limenelo: cifukwa limenelo ada
puma ku nchito yace yonse imene Mulungu anailenga ndi kupanga.
4Imeneyo ndiyo mibadwo yao ya zakumwamba ndi dziko lapansi, pamene
zinalengedwa, tsiku lomwe Yehova Mulungu anapanga dziko lapansi ndi
zakumwamba. 5Ndi zomera zonse za m'munda zisanakhale m'dziko lapansi,
ndiponso matherere onse a m'munda asanamere; cifukwa Yehova Mulungu
sanabvumbitsire mvula pa dziko lapansi, ndipo panalibe munthu wakulima
nthaka; 6kama inakwera nkhungu yoturuka pa dziko lapansi, niithirira ponse
pamwamba pa nthaka. 7Ndipo Yehova Mulungu anaumba munthu ndi dothi
lapansi, nauzira mpweya wa moyo m'mphuno mwace; munthuyo nakhala
wamoyo.

Pokhala pace pa munthu

8Ndipo Yehova Mulungu anabzala m'munda ku Edene cakum'mawa;
momwemo ndipo adaika munthu adamuumbayo. 9Ndipo Yehova Mulungu
anameretsa m'nthaka mitengo yonse yokoma m'maso ndi yabwino kudya;
ndiponso mtengo wa moyo pakati pa mundapo, ndi mtengo wakudziwitsa
zabwino ndi zoipa. 10Ndipo unaturuka m'Edene mtsinje wakuthirira
m'mundamo, m'menemo ndipo unalekana nucita miyendo inai. 11Dzina la
wakuyamba ndi Pisoni: umenewo ndiwo wozungulira dziko lonse la Havila,
m'mene muli golidi; 12golidi wa dziko ali wabwino; ndimonso muli bedola ndi
mwala wasohamu. 13Dzina la mtsinje waciwiri ndi Gihoni: umenewo ndiwo
wozungulira dziko lonse la Kusi. 14Dzina la mtsinje wacitatu ndi Hidikeli:
umenewo ndiwo wakuyenda ca kum'mawa kwace kwa Asuri. Mtsinje wacinai
ndi Pirate. 15Ndipo Yehova Mulungu anatenga munthuyo, namuika iye
m'munda wa Eriene kuti aulime nauyang'anire. 16Ndipo Yehova Mulungu
anamuuza munthuyo, nati, Mitengo yonse ya m'munda udyeko; 17koma
mtengo wakudziwitsa zabwino ndi zoipa, usadye umenewo; cifukwa tsiku
lomwe udzadya umenewo udzafa ndithu.
18Yehova Mulungu ndipo anati, Si kwabwino kuti munthuakhale yekha;
ndidzampangira womthangatira iye. 19Ndipo Yehova Mulungu anaumba ndi
nthaka zamoyo zonse za m'thengo, ndi mbalame zonse za m'mlengalenga;
ndipo anapita nazo kwa Adamu kuti aone maina omwe adzazicha; ndipo maina
omwe onse anazicha Adamu zamoyo zonse, omwewo ndiwo maina
ao. 20Adamu ndipo anazicha maina zinyama zonse, ndi mbalame za
m'mlengalenga ndi zamoyo zonse za m'thengo: koma kwa Adamu
sanapezedwa womthangatira iye. 21Koma Yehova Mulungu anamgonetsa
Adamu tulo tatikuru, ndipo anagona: ndipo anatengako nthiti yace imodzi,
natsekapo ndi mnofu pamalo pace: 22ndipo nthitiyo anaicotsa Yehova Mulungu
mwa Adamu anaipanga mkazi, ndipo ananka naye kwa Adamu. 23Ndipo anati
Adamu, Uyu tsopano ndiye pfupa la mafupa anga, ndi mnofu wa mnofu wanga;
ndipo adzachedwa Mkazi, cifukwa anamtenga mwa mwamuna. 24Cifukwa
cotero mwamuna adzasiya atate wace ndi amace nadzadziphatika kwa mkazi

wace: ndipo adzakhala thupi limodzi. 25Onse awiri ndipo anali amarisece, mwamuna ndi mkazi wace, ndipo analibe manyazi.

Genesis 3

Kucimwa kwa Adamu ndi Hava

1Ndipo njoka inali yakucenjera yoposa zamoyo zonse za m'thengo zimene
anazipanga Yehova Mulungu, Ndipo inati kwa mkaziyo, Ea! kodi anatitu
Mulungu, Usadye mitengo yonse ya m'mundamu? 2Mkaziyo ndipo anati kwa
njoka, Zipatso za mitengo ya m'mundamu tidye. 3Koma zipatso za mtengo
umene uti m'kati mwa munda, Mulungu anati, Musadye umenewo, musakhudze
umenewo, mungadzafe. 4Njokayo ndipo inati kwa mkaziyo, Kufa
simudzafai; 5cifukwa adziwa Mulungu kuti tsiku limene mukadya umenewo,
adzatseguka maso anu, ndipo mudzakhala ngati Mulungu, wakudziwa zabwino
ndi zoipa. 6Ndipo pamene anaona mkaziyo kuti mtengo unali wabwino kudya,
ndi kuti unali wokoma m'maso, mtengo wolakalakika wakupatsa nzeru,
anatenga zipatso zace, nadya, napatsanso mwamuna wace amene ali nave,
nadya iyenso, 7Ndipo anatseguka maso ao a onse awiri, nadziwa kuti anali
amarisece: ndipo adasoka masamba amkuyu, nadzipangira mateweta. 8Ndipo
anamva mau a Yehova Mulungu alinkuyendayenda m'munda nthawi
yamadzulo: ndipo anabisala Adamu ndi mkazi wace pamaso pa Yehova
Mulungu pakati pa mitengo ya m'munda. 9Ndipo Yehova Mulungu anaitana
mwamunayo nati kwa iye, Uli kuti? 10Ndipo anati, Ndinamva mau anu
m'mundamu, ndipo ndinaopa cifukwa ndinali wamarisece ine; ndipo
ndinabisala. 11Ndipo anati, Ndani anakuuza iwe kuti uli wamarisece? Kodi
wadya za mtengo uja, umene ndinakuuza iwe kuti usadye? 12Ndipo anati
mwamunayo, Mkazi amene munandipatsa ine kuti akhale ndi ine, ameneyo
anandipatsa ine za mtengo, ndipo ndinadya. 13Ndipo Yehova Mulungu anati
kwa mkaziyo, Ciani cimene wacitaci? Ndipo anati mkaziyo, Njoka inandinyenga
ine, ndipo ndinadya. 14Ndipo anati Yehova Mulungu kwa njokayo, Cifukwa kuti
wacita ici, wotembereredwa ndiwe wopambana ndi zinyama zonse ndi zamoyo
zonse za m'thengo: uziyenda ndi pamimba pako, uzidya pfumbi masiku onse a
moyo wako: 15ndipo ndidzaika udani pakati pa iwe ndi mkaziyo, ndi pakati pa
mbeu yako ndi mbeu yace; ndipo idzalalira mutu wako, ndipo iwe udzalalira
citende cace. 16Kwa mkaziyo ndipo anati, Ndidzacurukitsa kusauka kwako ndi
potenga mimba pako; udzasauka pakubala: udzakhumba mwamuna wako,
ndipo iye adzakulamulira iwe. 17Kwa Adamu ndipo anati, Cifukwa kuti wamvera
mau a mkazi wako, nudya za mtengo umene ndinakuuza iwe kuti, Usadyeko;
nthaka ikhale yotembereredwa cifukwa ca iwe; m'kusauka udzadyako masiku
onse a moyo wako: 18minga ndi mitula idzakubalira iwe; ndipo udzadya therere
la m'thengo: 19m'thukuta la nkhope yako udzadya cakudya, kufikira kuti
udzabwerera kunthaka: cifukwa kuti m'menemo unatengedwa: cifukwa kuti
ndiwe pfumbi, ndi kupfumbiko udzabwerera. 20Ndipo mwamuna anamucha
dzina la mkazi wace, Hava; cifukwa ndiye amace wa amoyo onse. 21Yehova
Mulungu ndipo anapangira Adamu ndi mkazi wace maraya azikopa, nawabveka
iwo.

22Ndipo anati Yehova Mulungu, Taonani, munthuyo akhala ngati mmodzi wa
ife, wakudziwa zabwino ndi zoipa: ndipo tsopano kuti asatambasule dzanja lace
ndi kutenga za mtengo wa moyo, ndi kudya, ndi kukhala ndi moyo nthawi
zonse, 23Yehova Mulungu anamturutsa iye m'munda wa Edene, kuti alime
nthaka m'mene anamtenga iye. 24Ndipo anamuingitsa munthuyo; nakhazika

Makerubi ca kum'mawa kwace kwa munda wa Edene, ndi lupanga lamoto lakuzungulira ponsepo, lakusunga njira ya ku mtengo wa moyo.

Genesis 4

Kaini ndi Abele. Kuphedwa koyamba

1Ndipo mwamunayo anadziwa mkazi wace Hava: ndipo anatenga pakati,
nabala Kaini, ndipo anati, Ndalandira munthu kwa Yehova. 2Ndipo anabalanso
mphwace Abele. Abele anakhala mbusa wa nkhosa, koma Kaini anali wakulima
nthaka. 3Ndipo panali atapita masiku, Kaini anatenga zipatso za nthaka,
nsembe ya kwa Yehova. 4Ndiponso Abele anatenga iyenso mwana woyamba
wa nkhosa zace ndi mafuta omwe. Yehova ndipo anayang'anira Abele ndi
nsembe yace: 5koma sanayang'anira Kaini ndi nsembe yace. Kaini ndipo
anakwiya kwambiri, niigwa nkhope yace. 6Ndipo Yehova anati kwa Kaini,
Ukwiyiranji? Yagweranji nkhope yako? 7Ukacita zabwino, sudzalandiridwa
kodi? Ukaleka kucita zabwino, ucimo ubwatama pakhomo: kwa iwe kudzakhala
kulakalaka kwace, ndipo iwe udzamlamulira iye. 8Kaini ndipo ananena ndi
Abele mphwace. Ndipo panali pamene anali kumunda, Kaini anamuukira Abele
mphwace, namupha, 9Yehova ndipo anati kwa Kaini, Ali kuti Abele mphwako?
Ndipo anati, Sindidziwai: kodi ndine woyang'anira mphwanga? 10Ndipo anati,
Wacita ciani? Mau a mwazi wa mphwako andipfuulira Ine kunthaka. 11Tsopano
ndiwe wotembereredwa kunthaka, Imene inatsegula pakamwa pace kulandira
pa dzanja lako mwazi wa mphwako: 12pamene udzalima panthaka
siidzaperekanso kwa iwe mphamvu yace: udzakhala wothawathawa ndi
woyendayenda pa dziko lapansi. 13Ndipo Kaini anati kwa Yehova, Kulangidwa
kwanga nkwakukuru kosapiririka. 14Taonani, mwandiingitsa ine lero lomwe
padziko; ndi pankhope panu ndidzabisika; ndipo ndidzakhala wothawathawa ndi
woyendayenda pa dziko lapansi; ndipo kudzatero kuti onse akundipeza
adzandipha. 15Ndipo Yehova anati kwa iye, Cifukwa cace ali yense amene
adzapha Kaini kudzabwezedwa kwa iye kasanu ndi kawiri. Ndipo Yehova
anaika icizindikiro pa Kaini, kuti asamuphe ali yense akampeza.

Mbumba ya Kaini

16Ndipo Kaini anaturuka pamaso pa Yehova, ndipo anakhalam'dziko la Nodi,
kum'mawa kwace kwa Edene. 17Ndipo Kaini anamdziwa mkazi wace; ndipo
anatenga pakati, nabala Enoke: ndipo anamanga mudzi, naucha dzina lace la
mudziwo monga dzina la mwana wace, Enoke. 18Kwa Enoke ndipo kunabadwa
Irade; Irade ndipo anabala Mehuyaeli; Mehuyaeli ndipo anabala Metusaeli;
Metusaeli ndipo anabala Lameke. 19Ndipo Lameke anadzitengera yekha akazi
awiri: dzina lace la wina ndi Ada, dzina lace la mnzace ndi Zila. 20Ndipo Ada
anabala Yabala; iye ndiye atate wao wa iwo okhala m'mahema, akuweta
ng'ombe, 21Ndi dzina la mphwace ndilo Yubala; iye ndiye atate wao wa iwo
oyimba zeze ndi citoliro. 22Ndipo Zila, iyenso anabala Tubala-Kaini, mwini
wakuphunzitsa amisiri onse a mkuwa ndi a citsulo; mlongo wace wa Tubala-
Kaini ndi Nama. 23Lameke ndipo anati kwa akazi ace:

Tamvani mau anga, Ada ndi Zila;
Inu akazi a Lameke, mverani kunena kwanga:
Ndapha munthu wakundilasa ine,
Ndapha mnyamata wakundiphweteka ine,
24Ngati Kaini adzabwezeredwa kasanu ndi kawiri,
Koma Lameke makumi asanu ndi awiri.

Kubadwa kwa Seti

25Ndipo Adamu anadziwanso mkazi wace; ndipo anabala mwana wamwamuna, namucha dzina lace Seti: Cifukwa, nati iye, Mulungu wandilowezera ine mbeu yina m'malo mwa Abele amene Kaini anamupha, 26Ndiponso kwa Seti, kwa iye kunabadwamwana wamwamuna: anamucha dzina lace Enosi: pomwepo anthu anayamba kuchula dzina la Yehova.

Genesis 5

Mbumba ya Seti

1Ili ndi buku la mibadwo ya Adamu. Tsiku lomwe Mulungu analenga munthu
anamlenga m'cifanizo ca Mulungu; 2anawalenga iwo mwamuna ndi mkazi,
nawadalitsa iwo nacha mtundu wao anthu, tsiku lomwe anawalenga
iwo. 3Ndipo Adamu anakhala ndi moyo zaka zana limodzi kudza makumi atatu,
nabala mwana wamwamuna m'cifanizo cace; namucha dzina lace
Seti. 4Masiku ace Adamu atabala Seti, anali zaka mazana asanu ndi atatu;
ndipo anabala ana amuna ndi akazi. 5Masiku ace onse anakhala ndi moyo
Adamu anali zaka mazana asanu ndi anai, kudza makumi atatu; ndipo
anamwalira.
6Ndipo Seti anakhala ndi moyo zaka zana kudza zisanu, nabala Enosi; 7ndipo
Seti anakhala ndi moyo, atabala Enosi, zaka mazana asanu ndi atatu kudza
zisanu ndi ziwiri: ndipo anabala ana amuna ndi akazi: 8masiku ace onse a Seti
anali zaka mazana asanu ndi anai kudza khumi ndi ziwiri; ndipo anamwalira.
9Ndipo Enosi anakhala ndi moyo zaka makumi asanu ndi anai, nabala
Kenani; 10ndipo anakhala ndi moyo Enosi, atabala Kenani, zaka mazana asanu
ndi atatu kudza khumi ndi zisanu: ndipo anabala ana amuna ndi
akazi. 11Masiku ace onse a Enosi anali mazana asanu ndi anai kudza zisanu;
ndipo anamwalira.
12Ndipo Kenani anakhala ndi moyo zaka makumi asanu ndi awiri, ndipo
anabala Mahalalele: 13ndipo Kenani anakhala ndi moyo, atabala Mahalalele
zaka mazana asanu ndi atatu kudza makumi anai, ndipo anabala ana amuna
ndi akazi; 14masiku ace onse a Kenani anali zaka mazana asanu ndi anai
kudza khumi; ndipo anamwalira.
15Ndipo Mahalalele anakhala ndi moyo zaka makumi asanu ndi limodzi kudza
zisanu, nabala Yaredi; 16ndipo Mahalalele anakhala ndi moyo, atabala Yaredi,
zaka mazana asanu ndi atatu kudza makumi atatu, nabala ana amuna ndi
akazi: 17masiku ace onse a Mahalalele anali zaka mazana asanu ndi atatu
kudza makumi asanu ndi anai ndi zisanu; ndipo anamwalira.
18Ndipo Yaredi anakhala ndi moyo zaka zana kudza makumi asanu ndi limodzi
ndi ziwiri, nabala Enoke; 19ndipo Yaredi anakhala ndi moyo, atabala Enoke,
zaka mazana asanu ndi atatu, nabala ana amuna ndi akazi; 20masiku ace onse
a Yaledi anali zaka mazana asanu ndi anai kudza maitumi asanu ndi limodzi ndi
ziwiri: ndipo anamwalira.
21Ndipo Enoke anakhala ndi moyo zaka makumi asanu ndi limodzi kudza
zisanu, nabala Metusela: 22ndipo Enoke anayendabe ndi Mulungu, atabala
Metusela, zaka mazana atatu, nabala ana amuna ndi akazi; 23masiku ace onse
a Enoke anali mazana atatu kudza makumi asanu ndi limodzi ndi
zisanu; 24ndipo Enoke anayendabe ndi Mulungu; ndipo panalibe iye; pakuti
Mulungu anamtenga.
25Ndipo Metusela anakhala ndi moyo zaka zana kudza makumi asanu ndi atatu
ndi zisanu ndi ziwiri, nabala Lameke; 26ndipo Metusela anakhala ndi moyo,
atabala Lameke, zaka mazana asanu ndi awiri kudza makumi asanu ndi atatu
ndi ziwiri, nabala ana amuna ndi akazi: 27masiku ace onse a Metusela anali
mazana asanu ndi anai kudza makumi asanu ndi limodzi kudza zisanu ndi zinai;
ndipo anamwalira.

28Ndipo Lameke anakhala ndi moyo zaka zana kudza makumi asanu ndi atatu ndi ziwiri, nabala mwana wamwamuna; 29namucha dzina lace Nowa, ndi kuti, Yemweyu adzatonthoza mtima wathu pa nchito zathu zobvuta za manja athu, cifukwa ca nthaka imene anaitemberera Yehova; 30ndipo Lameke anakhala ndi moyo atabala Nowa, zaka mazana asanu kudza makumi asanu ndi anai ndi zisanu, nabala ana amuna ndi akazi: 31masiku ace onse a Lameke anali zaka mazana asanu ndi awiri kudza makumi asanu ndi awiri; ndipo anamwa lira.
32Ndipo Nowa anali wa zaka mazana asanu; ndipo Nowa anabala Semu ndi Hamu ndi Yafeti.

Genesis 6

Kulowerera kwa mtundu wa anthu

1Ndipo panali pamene anthu anayamba kucuruka padziko, ndi ana akazi
anawabadwira iwo, 2kuti ana amuna a Mulungu anayang'ana ana akazi a
anthu, kuti iwo anali okongola; ndipo anadzitengera okha akazi onse amene
anawasankha. 3Ndipo anati Yehova, Mzimu wanga sudzakangana ndi anthu
nthawi zonse, cifukwa iwonso ndiwo thupi lanyama: koma masiku ace
adzakhala zaka zana limodzi kudza makumi awiri. 4Pa dziko lapansi panali
anthu akurukuru masiku omwewo ndiponso pambuyo pace, ana amuna a
Mulungu atalowa kwa ana akazi a anthu, ndipo anabalira iwo ana, amenewo
ndiwo anthu amphamvu akalekale, anthu omveka. 5Ndipo anaona Yehova kuti
kuipa kwa anthu kunali kwakukuru pa dziko lapansi, ndiponso kuti ndingaliro
zonse za maganizo a mitima yao zinali zoipabe zokhazokha. 6Ndipo Yehova
anamva cisoni cifukwa anapanga munthu pa dziko lapansi, ndipo anabvutika
m'mtima mwace. 7Ndipo anati Yehova, Ndidzafafaniza anthu amene
ndawalenga pa dziko lapansi; anthu, ndi nyama, ndi zokwawa, ndi mbalame za
m'mlengalenga: pakuti ndimva cisoni cifukwa ndapanga izo. 8Koma Nowa
anapeza ufulu pamaso pa Yehova.

9Mibadwoya Nowandiiyi: Nowa anali munthu wolungama ndi wangwiro
m'mibadwo yace; Nowa anayendabe ndi Mulungu. 10Ndipo Nowa anabala ana
amuna atatu, Semu, Hamu ndi Yafeti. 11Ndipo dziko lapansi linabvunda
pamaso pa Mulungu, dziko lapansi ndipo linadzala ndi ciwawa. 12Ndipo
Mulungu anaona dziko lapansi, ndipo taonani, linabvunda; pakuti anthu onse
anabvunditsa njira yao pa dziko lapansi.

Cigumula

13Ndipo Mulungu anati kwa Nowa, Cimariziro cace ca anthu onse cafika
pamaso panga; pakuti dziko lapansi ladzala ndi ciwawa cifukwa ca iwo; taonani,
ndidzaononga iwo pamodzi ndi dziko lapansi. 14Udzipangire wekha cingalawa
ca mtengo wanjale; upangemo zipinda m'cingalawamo, ndipo upake ndi utoto
m'kati ndi kunja. 15Kupanga kwace ndi kotere: m'litari mwace mwa cingalawa
mikono mazana atatu, m'mimba mwace mikono makumi asanu, m'msinkhu
mwace mikono makumi atatu. 16Uike zenera m'ciogalawaco, ulimarize ndi
kusiya mkono umodzi pamwamba pace: khomo la cingalawa uike m'mbali
mwace; nucipange ndi nyumba yapansi, ndi yaciwiri, ndi yacitatu. 17Ndine,
taonani, ndipo Ine ndidzadzetsa cigumula ca madzi pa dziko lapansi, kuti
cionooge zamoyo zonse, m'mene muli mpweya wa moyo pansi pa thambo;
zinthu zonse za m'dziko lapansi zidzafa. 18Koma ndidzakhazikitsa ndi iwe
pangano langa; ndipo udzalowa m'cingalawamo iwe ndi ana ako ndi mkazi
wako, ndi akazi a ana ako pamodzi ndi iwe. 19Ndipo zonse zokhala ndi moyo,
ziwiri ziwiri za mtundu wao ulowetse m'cingalawamo, kuti zikhale ndi moyo
pamodzi ndi iwe; zikhale zamphongo ndi zazikazi. 20Za mbalame monga mwa
mitundu yao, ndi zinyama monga mwa mitundu yao, ndi zokwawa zonse za
dziko lapansi monga mwa mitundu yao, ziwiri ziwiri monga mwa mitundu yao,
zidzadza kwa iwe kuti zikhale ndi moyo. 21Ndipo iwe udzitengereko wekha
zakudya zonse zodyedwa, oudzisonkhanitsire izi wekha: ndipo zidzakhala
zakudya za iwe ndi za iwo. 22Cotero anacita Nowa, monga mwa zonse
anamlamulira iye Mulungu, momwemo anacita.

Genesis 7

Nowa ndi banja lace alowa m'cingalawa

1Ndipo anati Yehova kwa Nowa, Talowani, iwe ndi a ku nyumba ako onse
m'cingalawamo; cifukwa ndakuona iwe kuti uli wolungama pamaso panga
m'mbadwo uno. 2Nyama zonse zodyedwa udzitengereko wekha zisanu ndi
ziwiri, zisanu ndi ziwiri, yamphongo ndi yaikazi yace; ndi nyama zosadyedwa
ziwiri ziwiri yamphongo ndi yaikazi yace. 3Ndiposo mbalame za kumlengalenga
zisanu ndi ziwiri, zisanu ndi ziwiri, yaimuna ndi yaikazi, kuti mbeu ikhale ndi
moyo pa dziko lonse lapansi. 4Pakuti akapita masiku asanu ndi awiri Ine
ndidzabvumbitsa mvula pa dziko lapansi masiku makumi anai usana ndi usiku;
ndi zinthu zamoyo zonse zomwe ndazipanga ndidzaziononga pa dziko
lapansi, 5Ndipo anacita Nowa monga mwa zonse anamlamulira iye Yehova.
6Ndipo Nowa anali wa zaka mazana asanu ndi limodzi, pamene cigumula ca
madzi cinali pa dziko lapansi. 7Ndipo analowa Nowa ndi ana ace ndi mkazi
wace ndi akazi a ana ace m'cingalawamo, cifukwa ca madzi a
cigumula. 8Nyama zodyedwa ndi nyama zosadyedwa, ndi mbalame, ndi zonse
zokwawa pansi, 9zinalowa ziwiri ziwiri kwa Nowa m'cingalawamo, yamphongo
ndi yaikazi, monga momwe Mulungu anamlamulira Nowa. 10Ndipo panali
pamene anapita masiku asanu ndi awiri, madzi a cigumula anali pa dziko
lapansi. 11Caka ca mazana asanu ndi limodzi ca moyo wa Nowa, mwezi
waciwiri, tsiku la khumi ndi asanu ndi awiri la mwezi, tsiku lomwelo akasupe
onse a madzi akuru anasefuka, ndi mazenera a kumwamba
anatseguka. 12Ndipo mvula inali pa dziko lapansi masiku makumi anai usana
ndi usiku. 13Tsiku lomwelo analowa m'cingalawamo Nowa, ndi Semu, ndi
Hamu, ndi Yafeti, ana a Nowa, ndi mkazi wace wa Nowa, ndi akazi atatu a ana
ace pamodzi nao: 14iwo, ndi zamoyo zonse monga mwa mitundu yao, ndi
zinyama zonse monga mwa mitundu yao, zokwawa zonse zokwawa pa dziko
lapansi monga mwa mitundu yao, ndi zouluka zonse monga mwa mitundu yao,
ndi mbalame zonse za mitundu mitundu. 15Ndipo zinalowa kwa Nowa
m'cingalawamo ziwiri ziwiri zamoyo zonse, m'mene muli mpweya wa
moyo. 16Zimene zinalowazo, zinalowa yamphongo ndi yaikazi zamoyo zonse,
monga momwe Mulungu anamlamulira iye: ndipo Yehova anamtsekera
iye. 17Ndipo cigumula cinali pa dziko lapansi masiku makumi anai: ndipo madzi
anacuruka natukula cingalawa, ndipo cinakwera pamwamba pa dziko
lapansi. 18Ndipo madzi anapambana, nacuruka ndithu pa dziko lapansi, ndipo
cingalawa cinayandama pamadzi. 19Ndipo madzi anapambana ndithu pa dziko
lapansi; anamizidwa mapiri atari onse amene anali pansi pa thambo
lonse. 20Madzi anapambana ndithu nakwera mikono khumi ndi isanu:
namizidwa mapiri, 21Ndipo zinafa zamoyo zonse zoyenda pa dziko lapansi,
zouluka, ndi nyama, ndi zamoyo, ndi zokwawa zonse zakukwawa pa dziko
lapansi, ndi anthu onse: 22zonse zimene m'mphuno zao munali mpweya wa
maimu wa moyo, zonse zinali pamtunda, zinafa. 23Ndipo zinaonongedwa
zamoyo zimene zonse zinali pa dziko lapansi, anthu, ndi nyama, ndi zokwawa,
ndi mbalame za m'mlengalenga; ndipo zinaonongedwa pa dzikolapansi:
anatsala Nowayekha ndi amene anali pamodzi naye m'cingalawa. 24Ndipo
anapambana madzi pa dziko lapansi masiku zana kudza makumi asanu.

Genesis 8

Nowa aturuka m'cingalawa

1Ndipo Mulungu anakumbukira Nowa ndi zamoyo zonse, ndi nyama zonse
zimene zinali pamodzi naye m'cingalawamo; ndipo Mulungu anapititsa mphepo
pa dziko lapansi, naphwa madzi; 2ndipo anatsekedwa akasupe a madzi akuru
ndi mazenera a kumwamba, niletsedwa mvula ya kwuwamba; 3ndipo madzi
anaphweraphwerabe pa dziko lapansi: pamene anatha masiku zana limodzi
kudza makumi atatu madzi anacepa. 4Ndipo cingalawa cinaima pa mapiri a
Ararati, mwezi wacisanu ndi ciwiri, tsiku lakhumi ndi asanu ndi awiri la
mwezi. 5Ndipo madzi analinkucepa kufikira mwezi wakhumi; mwezi wakhumi
tsiku loyamba mwezi ndipo padaoneka mitu ya mapiri.
6Ndipo panali atapita masiku makumi anai, Nowa anatsegula pa zenera la
cingalawa limene analipanga: 7ndipo anaturutsa khungubwe, ndipo anaturuka
kunka kwina ndi kwina kufikira adaphwa madzi pa dziko lapansi, 8Ndipo
anaturutsa njiwa imcokere, kuti aone kapena madzi anaphwa pamwamba pa
dziko lapansi; 9koma njiwayo siinapeza popondapo phazi lace, nibwera kwa iye
kucingalawako, pakuti madzi analipo pa dziko lonse lapansi; ndipo anaturutsa
dzanja lace, naitenga, nailowetsa kwa iye m'cingalawamo. 10Ndipo analinda
masiku ena asanu ndi awiri; naturutsanso njiwayo m'cingalawamo; 11ndipo
njiwa inadza kwa iye madzulo; ndipo, taonani, m'kamwa mwace munali tsamba
lazitona lotyoledwa: ndipo anadziwa Nowa kuti madzi analimkuphwa pa dziko
lapansi. 12Ndipo analindanso masiku ena asanu ndi awiri; naturutsa njiwayo:
ndipo siinabweranso konse kwa iye. 13Ndipo panali caka ca mazana asanu ndi
limodzi kudza cimodzi, mwezi woyamba, tsiku loyamba mwezi, madzi anaphwa
pa dziko lapansi; ndipo Nowa anacotsa cindwi lace pacingalawa, nayang'ana,
ndipo taonani, padauma pa dziko lapansi. 14Mwezi waciwiri tsiku la makumi
awiri kudza asanu ndi awiri la mwezi, lidauma dziko lapansi.
15Mulungu ndipo ananena kwa Nowa, kuti, 16Turukamoni m'cingalawamo, iwe
ndi ana ako, ndi mkazi wako, ndi akazi a ana ako pamodzi ndi iwe. 17Turutsa
pamodzi ndi iwe zamoyo zonse ziti ndi iwe za nyama zonse, zouluka, ndi
zinyama, ndi zokwawa zonse zakukwawa pa dziko lapansi; kuti ziswane pa
dziko lapansi, zibalane, zicuruke pa dziko lapansi. 18Ndipo anaturuka Nowa ndi
ana ace, ndi mkazi wace, ndi akazi a ana ace, pamodzi naye: 19zinyama
zonse, zokwawa zonse, zouluka zonse, ndi zonse zokwawa pa dziko lapansi,
monga mwa mitundu yao, zinaturuka m'cingalawamo.

Nowa amanga guwa la nsembe

20Ndipo Nowa anamanga guwa la nsembe la Yehova; natengapo nyama
zodyedwa zonse ndi mbalame zodyedwa zonse napereka nsembe zopsereza
paguwapo. 21Ndipo Yehova anamva conunkhira cakukondweretsa; nati Yehova
m'mtima mwace, Sindidzatembereranso konse nthaka cifukwa ca munthu;
pakuti ndingaliro ya mtima wa munthu iri yoipa kuyambira pa unyamata wace;
sindidzaphanso konse zinthu zonse zamoyo, monga momwe
ndacitiramo. 22Pakukhalabe masiku a dziko lapansi, nthawi yakubzala ndi
yakukunkha, cisanu ndi mafundi, malimwe ndi msakasa, usana ndi usiku
sizidzalekai.

Genesis 9

Mulungu acita pangano ndi Nowa

1Ndipo Mulungu anadalitsa Nowa ndi ana ace, nati kwa iwo, Mubalane, mucuruke, mudzaze dziko lapansi. 2Kuopsya kwanu, ndi kucititsa mantha kwanu kudzakhala pa zinyama zonse za dziko lapansi, ndi pa zouluka zonse za m'mlengalenga; ndi pa zonse zokwawa pansi, ndi pa nsomba zonse za m'nyanja, zapatsidwa m'dzanja lanu. 3Zoyenda zonse zamoyo zidzakhala zakudya zanu; monga therere laliwisi ndakupatsani inu zonsezo. 4Koma nyama, m'mene muli moyo wace, ndiwo mwazi wace, musadye. 5Zoonatu mwazi wanu wa miyoyo yanu ndidzafuna; pa dzanja la zinyama zonse ndidzaufuna: ndi pa dzanja la munthu, pa dzanja la mbale wace wa munthu ndidzaufuna moyo wa munthu. 6Amene akhetsa mwazi wa munthu, ndi munthunso mwazi wace udzakhetsedwa: cifukwa m'cifanizo ca Mulungu Iye anampanga munthu. 7Ndi inu, mubalane, mucuruke; muswane pa dziko lapansi, nimucuruke m'menemo.

8Ndipo Mulungu ananena kwa Nowa ndi kwa ana ace pamodzi naye, kuti, 9Ndipo Ine, taonani, Ine ndikhazikitsa pangano langa pamodzi ndi inu, ndi mbeu zanu pambuyo panu; 10ndi zamoyo zonse ziti pamodzi ndi inu, zouluka, ng'ombe, ndi zinyama zonse za dziko lapansi, pamodzi ndi inu; zonse zoturuka m'cingalawa, zinyama zonse za dziko lapansi, 11Ndipo ndidzakhazikitsa pangano langa pamodzi ndi inu; zamoyo zonse sizidzamarizidwanso konse ndi madzi a cigumula; ndipo sikudzakhalanso konse cigumula cakuononga dziko lapansi. 12Ndipo anati Mulungu, Ici ndici cizindikiro ca pangano limene ndipangana ndi Ine ndi inu, ndi zamoyo zonse ziti pamodzi ndi inu, ku mibadwo mibadwo; 13ndiika Uta-wa-Leza wanga m'mtambomo, ndipo udzakhala cizindikiro ca pangano lopangana ndi Ine ndi dziko lapansi. 14Ndipo padzakhala popimba ndi mtambo Ine dziko lapansi, utawo udzaoneka m'mtambomo; 15ndipo ndidzakumbukira pangano langa limene liri ndi Ine ndi inu, ndi zamoyo zonse zokhala ndi moyo; ndipo madzi sadzakhalanso konse cigumula cakuononga zamoyo zonse. 16Ndipo utawo udzakhala m'mtambo; ndipo ndidzauyang'anira kuti ndikumbukire pangano lacikhalire liri ndi Mulungu ndi zamoyo zonse zokhala ndi moyo pa dziko lapansi. 17Ndipo Mulungu anati kwa Nowa, Ici ndici cizindikiro ca pangano ndalikhazikitsa popaogana ndi Ine ndi zamoyo zonse za pa dziko lapansi.

18Ndi ana amuna a Nowa amene anaturuka m'cingalawa ndiwo Semu, ndi Hamu, ndi Yafeti: Hamu ndiye atate wace wa Kanani. 19Amenewa ndiwo ana amuna atatu a Nowa: ndiwo anafalikira dziko lonse lapansi.

Kuledzera kwa Nowa

20Ndipo anayamba Nowa kukhala munthu wakulima nthaka, ndipo analima munda wamphesa: 21namwa vinyo wace, naledzera; ndipo anali wamarisece m'kati mwa bema wace. 22Ndipo Hamu atate wace wa Kanani, anauona umarisece wa atate wace, nauza abale ace awiri amene anali kunja. 23Semu ndi Yafeti ndipo anatenga copfunda, naciika pa mapewa ao a onse awiri, nayenda cambuyo, napfunditsa umarisece wa atate wao: nkhope zao zinali cambuyo, osaona umarisece wa atate ao. 24Nowa ndipo anauka kwa kuledzera kwace, nadziwa cimene anamcitira iye mwana wace wamng'ono. 25Ndipo anati,

Wotembereredwa ndi Kanani:
Adzakhala kwa abale ace kapolo wa akapolo:
26Ndipo anati:
Ayamikike Yehova, Mulungu wa Semu;
Kanani akhale kapolo wace. 27Mulungu akuze Yafeti,
Akhale iye m'mahema a Semu; Kanani akhale kapolo wace.
28Ndipo Nowa anakhala ndi moyo cigumula citapita, zaka mazana atatu kudza makumi asanu. 29Ndipo masiku onse a Nowa anali mazana asanu ndi anai kudza makumi asanu: ndipo anamwalira.

Genesis 10

Mbumba ya Nowa

1Mibadwo ya ana a Nowa, Semu, Hamu, ndi Yafeti, ndi iyi; kwa iwo ndipo
kunabadwa ana amuna, citapita cigumula cija. 2Ana amuna a Yafeti: Gomeri,
ndi Magogi, ndi Madai, ndi Yavani, ndi Tubala, ndi Mesheki, ndi Tirasi, 3Ndi ana
amuna a Gomeri: Asekenazo, ndi Rifata, ndi Togarma. 4Ndi ana amuna a
Yavani: Elisa, ndi Tarisisi, ndi Kitimu, ndi Dodanimu. 5Amenewo ndipo anagawa
zisi za amitundu m'maiko mwao, onse amene monga mwa cinenedwe cao; ndi
mwa mabanja ao, ndi m'mitundu yao.
6Ndi ana amuna a Hamu: Kusi, ndi Mizraimu, ndi Puti, ndi Kanani. 7Ndi ana
amuna a Kusi: Seba, ndi Havila, ndi Sabita, ndi Raama, ndi Sabiteka; ndi ana a
Raama: Sheba ndi Dedane. 8Ndipo Kusi anabala Nimrode; ndipo iye anayamba
kukhala wamphamvu pa dziko lapansi. 9Iye ndiye mpalu wamphamvu pamaso
pa Yehova: cifukwa cace kunanenedwa, Monga Nimrode mpalu wamphamvu
pamaso pa Yehova. 10Ndipo kuyamba kwace kwa ufumu wace kunali Babele,
ndi Ereke, ndi Akadi, ndi Kaline, m'dziko la Sinara. 11M'dziko momwemo iye
anaturuka kunka ku Ashuri, namanga Nineve, ndi mudzi wa Rehoboti, ndi
Kala, 12ndi Resene pakati pa Nineve ndi Kala: umenewo ndi mudzi
waukuru. 13Mizraimu ndipo anabala Ludimu, ndi Anamimu, ndi Lehabimu, ndi
Nafituhimu, 14ndi Patrusimu, ndi Kasiluhimu, m'menemo ndipo anaturuka
Afilisti, ndi Kafitorimu.
15Ndipo Kanani anabala Sidoni woyamba wace, ndi Heti: 16ndi Ajebusi, ndi
Aamori, ndi Agirigasi; 17ndi Ahivi, ndi Aariki, ndi Asini; 18ndi Aaravadi, ndi
Aazemari, ndi Ahamati; pambuyo pace pamenepo ndipo mabanja a Akanani
anafalikira. 19Ndipo malire a Akanani anayamba pa Sidoni, pakunka ku Gerari
ndi ku Gaza; pakunka ku Sodomu, ndi ku Gomora, ndi Adima, ndi Zeboimu,
kufikira ku Lasa. 20Amenewa ndi ana amuna a Hamu monga mwa mabanja ao,
mwa zinenedwe zao, m'maiko ao, m'mitundu yao.
21Ndiponso kwa Semu atate wa ana onse a Ebere, mkuru wa Yafeti, kwa iye
kunabadwa ana. 22Ana amuna a Semu; Elamu, ndi Ashuri, ndi Aripakasadi, ndi
Ludi, ndi Aramu. 23Ndi ana a Aramu: Uzi ndi Huli, ndi Getere, ndi
Masi. 24Aripakasadi ndipo anabala Sela; ndipo Sela anabala Ebere. 25Kwa
Ebere ndipo kunabadwa ana amuna awiri; dzina la wina ndi Pelege; cifukwa
kuti m'masiku ace dziko lapansi linagawanikana; dzina la mphwace ndi
Yokitani. 26Ndipo Yokitani anabala Alamodadi, ndi Selefe, ndi Hazaramaveti,
ndi Yera; 27ndi Hadorimu ndi Uzali, ndi Dikila; 28ndi Obali, ndi Abimaele, ndi
Sheva; 29ndi Ofiri ndi Havila, ndi obabi; onse amenewa ndi ana a
okitani. 30Kwao kunayamba pa Mesa pakunka ku Sefere phiri la
kum'mawa. 31Amenewa ndi ana a Semu, monga mwa mabanja ao, mwa
zinenedwe zao, m'maiko ao, m'mitundu yao.
32Amenewo ndi mabanja a ana a Nowa monga mwa mibadwo yao, m'mitundu
yao: ndi amenewo anagawanika mitundu pa dziko lapansi, citapita cigumula.

Genesis 11

Nsanja ya Babele

1Ndipo dziko lapansi linali la cinenedwe cimodzi ndi cilankhulidwe
cimodzi. 2Ndipo panali pamene anayendayenda ulendo kum'mawa, anapeza
cigwa m'dziko la Sinara, ndipo anakhala kumeneko. 3Ndipo ananenana wina
ndi wina, Tiyeni tipange njerwa, tiziocetse. Ndipo anali ndi njerwa naziyesa
miyala, ndi katondo anayesa matope. 4Ndipo anati, Tiyeni, timange mudzi ndi
nsanja, pamutu pace pafikire kumwamba; ndipo tidzipangire ife tokha dzina kuti
tisabalalike pa dziko lonse lapansi. 5Ndipo Yehova anatsikira kudzaona mudzi
ndi nsanja imene analinkumanga ana a anthu. 6Ndipo Yehova anati, Taonani,
anthu ali amodzi, ndipo onse ali naco cinenedwe cao cimodzi; ndipo ici ayamba
kucita: ndipo tsopano palibe kanthu kakuletsedwa nao kamene akafuna
kucita. 7Tiyeni, titsike, pomwepo tisokoneze cinenedwe cao, kuti wina
asamvere cinenedwe ca mnzace. 8Ndipo Yehova anabalalitsa iwo pa dziko
lonse lapansi, ndipo analeka kumanga mudzi. 9Cifukwa cace anacha dzina lace
Babele; pakuti kumeneko Yehova anasokoneza cinenedwe ca dziko lonse
lapansi; kuyambira pamenepo Yehova anabalalitsa iwo pa dziko lonse lapansi.

Mibadwo ya Semu

10Mibadwo ya Semu ndi iyi: Semu anali wa zaka zana limodzi ndipo anabala
Aripakasadi, citapita cigumula zaka ziwiri; 11ndipo Semu anakhala ndi moyo
zaka mazana asanu, atabala Aripakasadi, nabala ana amuna ndi akazi.
12Ndipo Aripakasadi anakhala ndi moyo zaka makumi atatu kudza zisanu,
nabala Sela; 13ndipo Aripakasadi anakhala ndi moyo zaka mazana anai kudza
zitatu, atabala Sela, nabala ana amuna ndi akazi.
14Ndipo Sela anakhala ndi moyo zaka makumi atatu, nabala Ebere; 15ndipo
Sela anakhala ndi moyo zaka mazana anai kudza zitatu, atabala Ebere, nabala
ana amuna ndi akazi.
16Ndipo Ebere anakhala ndi moyo zaka makumi atatu kudza zinai, nabala
Pelege; 17ndipo Ebere anakhala ndi moyo zaka mazana anai kudza makumi
awiri, atabala Pelege, nabala ana amuna ndi akazi.
18Ndipo Pelege anakhala ndi moyo zaka makumi atatu, nabala, Reu; 19ndipo
Pelege anakhala ndi moyo zaka mazana awiri kudza zisanu ndi zinai, atabala
Reu, nabala ana amuna ndi akazi.
20Ndipo Reu anakhala ndi moyo zaka makumi atatu kudza ziwiri, nabala
Serugi: 21ndipo Reu anakhala ndi moyo zaka mazana awiri kudza zisanu ndi
ziwiri, atabala Serugi, nabala ana amuna ndi akazi.
22Ndipo Serugi anakhala ndi moyo zaka makumi atatu, nabala Nahori: 23ndipo
Serugi anakhala ndi moyo zaka mazana awiri, atabala Nahori, nabala ana
amuna ndi akazi.
24Ndipo Nahori anakhala ndi moyo zaka makumi awiri kudza zisanu ndi zinai,
nabala Tera: 25ndipo ahori anakhala ndi moyo zaka zana limodzi kudza khumi
ndi zisanu ndi zinai, atabala Tera, nabala ana amuna ndi akazi.
26Ndipo Tera anakhala ndi moyo zaka makumi asanu ndi awiri, nabala Abramu,
ndi Nahori ndi Harana.
27Mibadwo ya Tera ndi iyi: Tera anabala Abramu, ndi Nahori, ndi Harana; ndipo
Harana anabala Loti. 28Ndipo anafa Harana pamaso pa atate wace Tera
m'dziko la kubadwa kwace, m'Uri wa kwa Akaldayo. 29Ndipo Abramu ndi

Nahori, anadzitengera okha akazi; dzina lace la mkazi wa Abramu ndilo Sarai; ndi dzina lace la mkazi wa Nahori ndilo Milika, mwana wace wa Harana, atate wace wa Milika, ndi atate wace wa Yisika. 30Koma Sarai anali wouma; analibe mwana. 31Ndipo Tera anatenga Abramu mwana wace wamwamuna, ndi Loti mwana wa Harana, mwana wace wamwamuna, ndi Sarai mpongozi wace, mkazi wa mwana wace Abramu; ndipo anaturuka pamodzi nao ku Uri wa kwa Akaldayo kuti amuke ku dziko la Kanani, ndipo anafika ku Harana, nakhala kumeneko. 32Masiku a Tera anali zaka mazana awiri kudza zisanu; ndipo anafa Tera m'Harana.

Genesis 12

Kuitanidwa kwa Abramu

1Ndipo Yehova anati kwa Abramu, Turuka iwe m'dziko lako, ndi kwa abale ako, ndi ku nyumba ya atate wako, kunka ku dziko limene ndidzakusonyeza iwe; 2ndipo ndidzakuyesa iwe mtundu waukuru, ndipo ndidzakudalitsa iwe, ndi kubukitsa dzina lako; nukhale iwe mdalitso; 3ndipo ndidzadalitsa amene akudalitsa iwe; ndi kutemberera iye amene akutemberera iwe; ndipo mwa iwe adzadalitsidwa mabanja onse a dziko lapansi, 4Ndipo anamuka Abramu monga Yehova ananena kwa iye, ndipo Loti anamuka pamodzi naye: ndipo Abramu anali wa zaka makumi asanu ndi awiri kudza zisanu, pamene anaturuka m'Harana. 5Ndipo Abramu anatenga Sarai mkazi wace, ndi Loti mwana wa mphwace, ndi cuma cao cimene anasonkhanitsa, ndi miyoyo imene anabala m'Harana; naturuka kunka ku dziko la Kanani, ndipo anadza ku dziko la Kanani. 6Ndipo Abramu anapitira m'dziko kufikira ku malo a Sekemu, kufikira ku mtengo wathundu wa ku More. Akanani anali m'dzikomo nthawi yomweyo. 7Ndipo Yehova anaonekera kwa Abramu nati, Ndidzapatsa mbeu yako dziko lino: pamenepo anammangira Yehova guwa la nsembe amene anamuonekera iye. 8Ndipo iye anacoka kumeneko kunka ku phiri la kum'mawa kwa Beteli, namanga hema wace; Beteli anali kumadzulo, ndi Ai anali kum'mawa: kumeneko ndipo anammangira Yehova guwa la nsembe, naitanira dzina la Yehova. 9Ndipo Abramu anayenda ulendo wace, nayendayenda kunka kumwela.

Abramu atsikira ku Aigupto

10Ndipo munali njala m'dzikomo, ndipo anatsikira Abramo ku Aigupto kukakhala kumeneko, cifukwa kuti njala inali yaikuru m'dziko m'menemo. 11Ndipo panali pamene anayandikira kulowa m'Aigupto, anati kwa Sarai mkazi wace, Taonani, ndidziwa kuti ndiwe mkazi wokongola maonekedwe ako; 12ndipo padzakhala pamene adzakuona iwe Aaigupto, adzati, Uyu ndi mkazi wace: ndipo adzandipha ine, koma iwe adzakuleka ndi moyo. 13Uzikanenatu, kuti iwe ndiwe mlongo wanga: kuti cidzakhala cabwino ndi ine, cifukwa ca iwe, ndi kuti moyo wanga usungike ndi iwe. 14Ndipo panali pamene Abramu analowa m'Aigupto, Aaigupto anaona kuti mkazi anali wokongola kwambiri. 15Ndipo akaronga ace a Farao anamuona iye, namyamikira iye kwa Farao; ndipo anamuka ndi mkazi kunyumba kwace kwa Farao. 16Ndipo anamcitira Abramu bwino cifukwa ca iyeyo; ndipo anali nazo nkhosa, ndi ng'ombe, ndi aburu, ndi akapolo, ndi adzakazi, ndi aburu akazi, ndi ngamila. 17Koma Yehova anabvutitsa Farao ndi banja lace ndi nthenda zazikuru cifukwa ca Sarai mkazi wace wa Abramu, 18Ndipo Farao anaitana Abramu, nati, Nanga nciani ici wandicitira ine? cifukwa canji sunandiuza ine kuti ndiye mkazi wako? 19Cifukwa canji unati, Ndiye mlongo wanga? Kotero ndinamtenga iye akhale mkazi wanga; tsopano suyu mkazi wako; mtenge nucoke. 20Ndipo Farao analamulira anthu ace za iye; ndipo anamperekeza iye m'njira ndi mkazi wace ndi zonse anali nazo.

Genesis 13

Abramu ndi Loti alekana

1Ndipo anakwera Abramu kucoka ku Aigupto, iye ndi mkazi wace, ndi zonse
anali nazo, ndi Loti pamodzi naye, kunka ku dziko la kumwera. 2Ndipo Abramu
anali wolemera ndithu ndi ng'ombe ndi siliva ndi golidi, 3Ndipo anankabe
ulendowace kucokera ku dziko la kumwera kunka ku Beteli, kufikira kumalo
kumene kunali hema wace poyamba paja, pakati pa Beteli ndi Ai; 4kumalo kwa
guwa la nsembe analimanga iye kumeneko, poyamba paja; ndipo pamenepo
Abramu anaitanira dzina la Yehova. 5Ndiponso Loti anayenda ndi Abramu anali
ndi nkhosa ndi ng'ombe ndi mahema. 6Ndipo dziko silinathe kuwakwanira iwo,
kuti akhale pamodzi: cifukwa kuti cuma cao cinali cambiri, ndipo sanathe
kukhala pamodzi. 7Ndipo panali ndeu, abusa a Abramu kudana ndi abusa a
Loti: Akanani ndi Aperezi ndipo analinkukhala nthawi yomweyo
m'dzikomo. 8Ndipo Abramu anati kwa Loti, Tisacite ndeu, ine ndi iwe, abusa
anga ndi abusa ako: cifukwa kuti ife ndife abale. 9Dziko lonse siliri pamaso
pako kodi? Ulekanetu ndi ine: ukanka iwe ku dzanja lamanzere, ine ndinka ku
dzanja lamanja: ukanka iwe ku dzanja lamanja, ine ndinka ku dzanja
lamanzere. 10Ndipo Loti anatukula maso ace nayang'ana cigwa conse ca
Yordano kuti conseco cinali ndi madzi ambiri, asanaononge Yehova Sodomu
ndi Gomora, monga munda wa Yehova, monga dziko la Aigupto pakunka ku
Zoari. 11Ndipo Loti anasankha cigwa conse ca Yordano; ndipo Loti anacoka
ulendo wace kunka kum'mawa: ndipo analekana wina ndi mnzace. 12Ndipo
Abramu anakhala m'dziko la Kanani, ndipo Loti anakhala m'midzi ya m'cigwa,
nasendeza hema wace kufikira ku Sodomu. 13Ndipo anthu a ku Sodomu anali
oipa ndi ocimwa kwambiri pamaso pa Yehova.

Mulungu alonjeza kwa Abramu kumpatsa Kanani

14Ndipo Yehova anati kwa Abramu, atalekana naye Loti, Tukulatu maso ako,
nuyang'anire kuyambira kumene uliko, kumpoto, ndi kumwela, ndi kum'mawa,
ndi kumadzulo: 15cifukwa kuti dziko lonse limene ulinkuona, ndidzakupatsa iwe
ndi mbeu yako nthawi yonse. 16Ndipo ndidzayesa mbeu yako monga pfumbi
lapansi: cotere kuti ngati munthu angathe kuwerenga pfumbi lapansi,
comweconso mbeu yako idzawerengedwa. 17Tauka, nuyendeyendc m'dzikoli
m'litari mwace ndi m'mimba mwace; cifukwa kuti ndidzakupatsa iwe
limenelo. 18Ndipo Abramu anasuntha hema wace nafika nakhala pa mitengo
yathundu ya pa Mamre, imene iri m'Hebroni, nammangira Yehova kumeneko
guwa la nsembe.

Genesis 14

Abramu alanditsa Loti

1Ndipo panali masiku a Amarafele mfumu ya Sinara, ndi Arioki mfumu ya
Elasara, ndi Kedorelaomere mfumu ya Elami, ndi Tidala mfumu ya Goimu, 2iwo
anathira nkhondo pa Bera mfumu ya Sodomu, ndi pa Birisa, mfumu ya Gomora,
ndi pa Sinabi mfumu ya Adima, ndi pa Semebere mfumu ya Ziboimu, ndi pa
mfumu ya Bela (kumeneko ndi ku Zoari). 3Onse amenewo anadziphatikana pa
cigwa ca Sidimu (pamenepo ndi pa nyanja yamcere). 4Zaka khumi ndi ziwiri iwo
anamtumikira Kedorelaomere, caka cakhumi ndi citatu anapanduka, 5Caka
cakhumi ndicinai ndipo anadza Kedorelaomere ndi mafumu amene anali naye,
nawakantha Arefai m'Aseteroti-kamaimu, ndi Azuzi m'Hamu, ndi Aemi
m'Savekiriataimu, 6ndi Ahori pa phiri lao Seiri kufikira ku Eliparana, kumene kuli
pacipululu. 7Ndipo anabwera nafika ku Eni-Misipati (ku meneko ndi ku Kadese),
nakantha dziko lonse la Aamaleki, ndiponse Aamori amene akhala m'Hazezoni-
tamara. 8Ndipo anaturuka mfumu ya Sodomu, ndi ya Gomora, ndi mfumu ya
Adima, ndi mfumu ya Zeboimu, ndi mfumu ya Bela (kumeneko ndi ku Zoari)
ndipo anawathira nkhondo m'cigwa ca Sidimu 9ndi Kedorelaomere mfumu ya
Elamu, ndi Tidala mfumu ya Goimu ndi Amarafele mfumu ya Sinara, ndi Arioki
mfumu ya Elasara; mafumu anai kugwirana ndi asanu. 10Cigwa ca Sidimu
cinali ndi zitengetenge tho; ndipo anathawa mafumu a ku Sodomu ndi Gomora
nagwa m'menemo: amene anatsala anathawira kuphiri. 11Ndipo anatenga
cuma conse ca Sodomu ndi Gomora ndi zakudya zao zonse, namuka. 12Ndipo
anagwira Loti mwana wa Abramu amene anakhala m'Sodomu, ndi cuma cace,
namuka. 13Ndipo anadza wina amene anapulumuka namuuza Abramu Mhebri;
ndipo iye analinkukhala pa mitengo yathundu ya pa Mamre M-amori, mkuru
wace wa Esakolo, ndi mkuru wace wa Aneri; amenewo ndiwo opangana naye
Abramu. 14Pamene anamva Abramu kuti mphwace anagwidwa, anaturuka
natsogolera anyamata ace opangika, obadwa kunyumba kwace, mazana atatu
kudza khumi ndi asanu ndi atatu, nawalondola kutikira ku Dani. 15Ndipo
anadzigawanizira iwo usiku, iye ndi anyamata ace, nawakantha, nawapitikitsa
kufikira ku Hoba, ndiko ku dzanja lamanzere la ku Damasiko. 16Ndipo
anabwera naco cuma conse, nabwera naye Loti yemwe ndi cuma cace, ndi
akazi ndi anthu omwe.

Melikizedeke adalitsa Abramu

17Ndipo anaturuka mfumu ya Sodomu kukomana naye, atabwera anatha
kuwakantha Kedorelaomere ndi mafumu amene anali naye, ku cigwa ca Save
(ndiko ku cigwa ca mfumu), 18Ndipo Melikizedeke mfumu ya ku Salemu,
anaturuka nao mkate ndi vinyo: iye ndiye wansembe wa Mulungu
Wamkurukuru. 19Ndipo anamdalitsa iye, nati, Abramu adalitsike ndi Mulungu
Wamkurukuru, mwini kumwamba ndi dziko lapansi; 20ayamikike Mulungu
Wamkurukuru amene wapereka adani ako m'dzanja lako. Ndipo anampatsa iye
limodzi la magawo khumi la zonse. 21Mfumu ya Sodomu ndipo inati kwa
Abramu, Ndipatse ine anthu, nutenge cuma iwe wekha. 22Ndipo Abramu anati
kwa mfumu ya Sodomu, Dzanja langa ndamtukulira Yehova, Mulungu
Wamkurukuru, mwini kumwamba ndi dziko lapansi, 23kuti sindidzatenga
ngakhale thonje ngakhale cingwe ca nsapato, ngakhale kanthu kali konse kako,
kuti unganene, Ndamlemeza Abramu; 24koma cokhaci anadya anyamata, ndi

gawo lao la anthu amene ananka pamodzi ndi ine, Aneri, Esikolo, ndi Mamre, iwo atenge gawo lao.

Genesis 15

Mulungu apangana ndi Abramu

1Zitapita izo, mau a Yehova anadza kwa Abramu m'masomphenya, kuti,
Usaope, Abramu, Ine ndine cikopa cako ndi mphotho yako yaikurukuru. 2Ndipo
Abramu anati, Ambuye Mulungu, mudzandipatsa ine ciani popeza ndine
wopanda mwana, ndi amene adzakhala mwini nyumba yanga ndiye Eliezere wa
ku Damasiko? 3Ndipo Abramu anati, Taonani, simunandipatse ine mbeu; ndipo,
taonani, wobadwa m'nyumba mwanga adzalowa m'malo mwanga. 4Ndipo,
taonani, mau a Yehova anadza kwa iye kuti, Uyu sadzakhala wakulowa m'malo
mwako; koma iye amene adzaturuka m'cuuno mwako, ndiye adzakhala
wakulowa m'malo mwako. 5Ndipo anamturutsa iye kunja, nati, Tayang'anatu
kumwamba, uwerenge nyenyezi, ngati ukhoza kuziwerenga zimenezo: ndipo
anati kwa iye, Zoterezo zidzakhala mbeuzako. 6Ndipo anakhulupirira Yehova,
ndipo kunayesedwa kwa iye cilungamo. 7Ndipo anatikwaiye, Ine ndine Yehova
amene ndinaturutsa iwe m'Uri wa kwa Akaldayo, kuti ndikupatse iwe dziko
limeneli likhale lako lako. 8Ndipo anati, Ambuye Mulungu, nanga ndidzadziwa
bwanji kuti lidzakhala colowa canga? 9Ndipo anati kwa iye, Kanditengere Ine
ng'ombe yaikazi ya zaka zitatu, ndi mbuzi yaikazi ya zaka zitatu, ndi tonde wa
zaka zitatu, ndi njiwa, ndi bunda. 10Ndipo anatenga iye zonse zimenezo,
nazidula pakati, naika bandu popenyana ndi linzace: koma mbalame
sanazidula. 11Pamene miimba inatsikira panyama, Abramu anaingitsa
iyo. 12Ndipo linalinkulowa dzuwa, ndi tulo tatikuru tinamgwera Abramu: ndipo
taonani, kuopsya kwa mdima waukuru kunamgwera iye. 13Ndipo anati kwa
Abramu, Dziwitsa ndithu kuti mbeu zako zidzakhala alendo m'dziko la eni,
nizidzatumikira iwo, ndipo iwo adzasautsa izo zaka mazana anai; 14ndiponso
mtunduwo adzautumikira, Ine ndidzauweruza: ndiponso pambuyo pace
adzaturuka ndi cuma cambiri. 15Ndipo iwe udzanka kwa makolo ako
m'mtendere; nudzaikidwa ndi ukalambawabwino. 16Koma iwo adzabweranso
kuno mbadwo wacinai: pakuti mphulupulu za Aamori sizinakwaniridwe. 17Ndipo
panali pamene litalowa dzuwa ndi kudza mdima, taonani, ng'anjo yofuka utsi
ndi muuni wamoto wapita pakati pa mabanduwo. 18Tsiku lomwelo Yehova
anapangana cipangano ndi Abramu, nati, Ndidzapatsa mbeu zako dziko ili,
kuyambira pa nyanja ya Aigupto kufikira pa nyanja yaikuru, nyanja ya
Firate: 19Akeni ndi Akenizi, Akadimoni, ndi Ahiti, ndi Aperezi, ndi Arefai, ndi
Aamori, ndi Akanani, ndi Agirigasi, ndi Ajebusi.

Genesis 16

Sara ndi Hagara

1Ndipo Sarai mkazi wace wa Abramu sanambalire iye mwana; ndipo anali ndi
mdzakazi, wa ku Aigupto, dzina lace Hagara. 2Ndipo Sarai anati kwa Abramu,
Taonanitu, Yehova anandiletsa ine kuti ndisabale: lowanitu kwa mdzakazi
wanga; kapena ndikalandire ndi iye ana. Ndipo Abramu anamvera mau a
Sarai. 3Ndipo Sarai mkazi wace wa Abramu anatenga Hagara mdzakazi wace
wa ku Aigupto, Abramu atakhala m'dziko la Kanani zaka khumi, nampereka iye
kwa Abramu mwamuna wace, kuti akhale mkazi wace. 4Ndipo analowa kwa
Hagara, ndipo iye anatenga pakati. Pamene anaona kuti anatenga pakati,
anapeputsa wakuka wace m'maso mwace. 5Ndipo Sarai anati kwa Abramu,
Kusauka kwanga kukhale pa iwe: ndakupatsa iwe mdzakazi wanga pamtima
pako; ndipo pakuona kuti anatenga pakati anandipeputsa ine m'maso mwace:
Yehova aweruze pakati pa iwe ndi ine. 6Koma Abramu anati kwa Sarai, Taona,
mdzakazi wako ali m'dzanja lako, umcitire iye cimene cikukomera m'maso
mwako. Ndipo Sarai anamsautsa iye, ndipo anathawa kumaso kwace. 7Ndipo
mthenga wa Yehova anampeza iye pa kasupe wa madzi m'cipululu, pa kasupe
wa pa njira ya ku Suri. 8Ndipo anati, Hagara, mdzakazi wace wa Sarai, ufumira
kuti? Unka kuti? Ndipo anati, Ndithawa ine kumaso kwace kwa wakuka wanga
Sarai. 9Ndipo mthenga wa Yehova anati kwa iye, Bwera kwa wakuka wako,
udzicepetse wekha pamanja pace. 10Ndipo mthenga wa Yehova anati kwa iye,
Ndidzacurukitsa ndithu mbeu zako, kuti unyinji wao sudzawerengeka.

Kubadwa kwa Ismayeli

11Ndipo mthenga wa Yehova anati kwa iye, Taona, uli ndi pakati, ndipo
udzabala mwana wamwamuna; nudzamucha dzina lace Ismayeli; cifukwa
Yehova anamva kusauka kwako. 12Ndipo iye adzakhala munthu wa m'thengo;
ndipo dzanja lace lidzakhala lotsutsana ndi anthu onse, ndi manja a anthu onse
adzakhala otsutsana naye: ndipo iye adzakhala pamaso pa abale ace
onse. 13Ndipo anacha dzina la Yehova amene ananena naye, Ndinu Mulungu
wakundiona ine; pakuti anati, Kodi kunonso ndayang'ana pambuyo pace pa iye
amene wakundiona ine? 14Cifukwa cace citsimeco cinachedwa Beerelahai-roi;
taonani ciri pakati pa Kadese ndi Berede. 15Ndipo Hagara anambalira
Abramumwana wamwamuna, ndipo Abramu anacha dzina la mwana wace
amene anambalira iye Hagara, lsmayeli. 16Ndipo Abramu anali wa zaka
makumi asanu ndi atatu kudza zisanu ndi cimodzi, pamene Hagara anambalira
Abramu Ismayeli.

Genesis 17

Dzina la Abramu lisinthika likhale Abrahamu

1Pamene Abramu anali wa zaka makumi asanu ndi anai kudza zisanu ndi zinai,
Yehova anamuonekera Abramu nati kwa iye, Ine ndine Mulungu
Wamphamvuyonse; yenda iwe pamaso panga, nukhale wangwiro. 2Ndipo
ndidzapangana pangano langa ndi Ine ndi iwe, ndipo ndidzacurukitsa iwe
kwambiri. 3Ndipo Abramu anagwa nkhope pansi, ndipo Yehova ananena naye
kuti, 4Koma Ine, taona, pangano langa liri ndi iwe, ndipo udzakhala iwe atate
wa khamu la mitundu. 5Sudzachedwanso dzina lako Abramu, koma dzina lako
lidzakhala Abrahamu; cifukwa kuti ndakuyesa iwe atate wa khamu la
mitundu. 6Ndipo ndikubalitsa iwe ndithu, ndipo ndidzakuyesa iwe mitundu,
ndipo mafumu adzaturuka mwa iwe. 7Ndipo ndidzalimbitsa pangano langa ndi
Ine ndi iwe pa mbeu zako za pambuyo pako m'mibadwo yao, kuti likhale
pangano la nthawi zonse, kuti ndikhale Mulungu wako ndi wa mbeu zako za
pambuyo pako. 8Ndipo ndidzakupatsa iwe ndi mbeu zako za pambuyo pako,
dziko la maulendo anu, dziko lonse la Kanani likhale lako nthawi zonse: ndipo
Ine ndidzakhala Mulungu wao.

Mulungu aika cizindikilo ca Kudulidwa

9Ndipo Mulungu anati kwa Abrahamu, Koma iwe, uzikumbukira pangano langa,
iwe ndi mbeu zako za pambuyo pako m'mibadwo yao. 10Ili ndi pangano langa
limene uzisunga pakati pa Ine ndi iwe ndi mbeu zako zapambuyo pako:
azidulidwa amuna onse a mwa inu. 11Muzidula khungu lanu; ndipo cidzakhala
cizindikiro ca pangano pakati pa Ine ndi inu. 12A masiku asanu ndi atatu
azidulidwa mwa inu, ana amuna onse m'mibadwo mwanu, amene abadwa
m'nyumba ndi amene agulidwa ndi ndalama kwa alendo ali onse, wosakhala
mwa mbeu zako. 13Azidulidwatu amene abadwa m'nyumba mwako ndi amene
agulidwa ndi ndalama zako: ndipo pangano langa lidzakhala m'thupi mwako
pangano losatha. 14Ndipo mwamuna wosadulidwa, wosadulidwa khungu lace
munthuyo amsadze mwa anthu a mtundu wace; waphwanya pangano langa.

D'zina la Sarai lisinthika likhale Sara

15Ndipo Mulungu anati kwa Abrahamu, Koma Sarai mkazi wako, usamcha
dzina lace Sarai, koma dzina lace ndi Sara. 16Ndipo ndidzamdalitsa iye,
ndiponso ndidzakupatsa iwe mwana wamwamuna wobadwa mwa iye, inde,
ndidzamdalitsa iye, ndipo adzakhala amace a mitundu, mafumu a anthu
adzaturuka mwa iye. 17Ndipo Abrahamu adagwa nkhope pansi, naseka, nati
m'mtima mwace, Kodi mwana adzabadwa kwa iye amene ali wa zaka zana?
Kodi Sara wa zaka makumi asanu ndi anai adzabala? 18Ndipo Abrahamu anati
kwa Mulungu, Ha! Ismayeli akhale ndi moyo pamaso panu! 19Ndipo Mulungu
anati, Koma Sara mkazi wako adzakubalira iwe mwana wamwamuna; ndipo
udzamucha dzina lace Isake; ndipo ndidzalimbikitsa nave pangano langa, kuti
likhale pangano la nthawi zonse, la ku mbeu zace za pambuyo pace. 20Koma
za Ismayeli, ndamvera iwe: taona, ndamdalitsa iye, ndipo ndidzamcurukitsa iye
ndithu; adzabala akaronga khumi ndi awiri, ndipo ndidzamuyesa iye mtundu
waukuru. 21Koma pangano langa ndidzalimbikitsa ndi Isake, amene Sara
adzakubalira iwe nthawi yomwe yino caka camawa. 22Ndipo analeka kunena
naye, ndipo Mulungu anakwera kucokera kwa Abrahamu. 23Ndipo Abrahamu
anatenga Ismayeli mwana wace ndi onse amene anabadwa m'nyumba mwace,

ndi onse, amene anagulidwa ndi ndalama zace, amuna onse a mwa anthu a kunyumba kwace kwa Abrahamu, nadula khungu lao tsiku lomwelo, monga Mulungu ananena naye. 24Ndipo Abrahamu anali wa zaka makumi asanu ndi anai kudza zisanu ndi zinai, pamene anadulidwa m'khungu lace. 25Ndipo Ismayeli mwana wace anali wa zaka khumi ndi zitatu pamene anadulidwa m'khungu lace. 26Tsiku lomwelo anadulidwa Abrahamu ndi Ismayeli mwana wace. 27Ndipo amuna onse a m'nyumba mwace obadwa m'nyumba, ndi ogulidwa ndi ndalama kwa alendo, anadulidwa pamodzi naye.

Genesis 18

Amithenga atatu amuonekera Abrahamu

1Ndipo Yehova anamuonekera iye pa mtengo yathundu ya ku Mamre, pamene
anakhala pa khomo la hema wace pakutentha dzuwa. 2Ndipo anatukula maso
ace, nayang'ana, taonani, anthu atatu anaima pandunji pace; pamene anaona
iwo, anawathamangira kucoka ku khomo la hema kukakomana nao, nawerama
pansi, nati, 3Mbuyanga, ngatitu ndikapeza ufulu pamaso panu, musapitiriretu
pa kapolo wanu; 4nditengetu madzi pang'ono, ndikusambitseni mapazi anu,
mupumule pansi pa mtengo; 5ndipo ndidzatenga cakudya pang'ono,
nimutonthoze mitima yanu; mutatero mudzapitirira, cifukwa mwafika kwa kapolo
wanu. Ndipo anati, Cita comweco monga momwe wanena. 6Ndipo Abrahamu
analowa msanga m'hema wace kwa Sara, nati, Konza msanga miyeso itatu ya
ufa wosalala, nuumbe, nupange mikate. 7Ndipo Abrahamu anafulumira kunka
kuzoweta, natenga kamwana ka ng'ombe kofewa ndi kabwino, napatsa
mnyamata, ndipo anafulumira kuphika. 8Ndipo anatenga mafuta amkaka, ndi
mkaka, ndi kamwana ka ng'ombe kamene anaphika, naziika patsogolo pao;
ndipo iye anaimirira iwo patsinde pa mtengo, ndipo anadya. 9Ndipo anati kwa
iye, Ali kuti Sara mkazi wako? Ndipo anati, Taonani m'hemamo. 10Ndipo anati,
Ndidzabwera kwa iwe ndithu pakufika nyengo yace; taonani Sara mkazi wako
adzakhala ndi mwana wamwamuna. Ndipo Sara anamva pakhomo pa hema
amene anali pambuyo pace. 11Koma Abrahamu ndi Sara anali okalamba, ana
pitirira masiku ao; ndipo kunaleka kwa Sara konga kumacita ndi akazi; 12ndipo
Sara anaseka m'mtima mwace, nati, Kodi ndidzakhala ndi kukondwa ine
nditakalamba, ndiponso mbuyanga ali wokalamba? 13Ndipo Yehova anati kwa
Abrahamu, Bwanji anaseka Sara, kuti, Kodi ndidzabala ine ndithu, ine amene
ndakalamba? 14Kodi ciripo cinthu comlaka Yehova? Pa nthawi yoikidwa
ndidzabwera kwa iwe, pakufika nyengo yace, ndipo Sara adzakhala ndi mwana
wamwamuna. 15Koma Sara anakana, nati, Sindinasekai; cifukwa anaopa,
Ndipo anati, lai; koma unaseka. 16Ndipo anthuwo anauka kucokera kumeneko
nayang'ana ku Sodomu; ndipo Abrahamu ananka nao kuwaperekeza. 17Ndipo
Yehova adati, Kodi ndidzabisira Abrahamu cimene ndicita? 18Pakuti Abrahamu
adzakhala ndithu wamkuru ndi wamphamvu, ndipo mitundu yonse ya dziko
lapansi idzadalitsika mwa iye? 19Cifukwa ndamdziwa iye kuti alamulire ana ace
ndi banja lace la pambuyo pace, kuti asunge njira ya Yehova, kucita cilungamo
ndi ciweruziro, kuti Yehova akamtengere Abrahamu comwe anamnenera
iye. 20Ndipo anati Yehova, Popeza kulira kwa Sodomu ndi Gomora kuli
kwakukuru, ndipo popeza kucimwa kwao kuli kulemera ndithu, 21ndidzatsikatu
ndikaone ngati anacita monse monga kulira kwace kumene kunandifikira: ngati
sanatero ndidzadziwa.

Abrahamu apempherera a ku Sodomu

22Ndipo anthuwo anatembenuka nacoka kumeneko, napita kunka ku Sodomu.
Koma Abrahamu anaimabe pamaso pa Yehova. 23Ndipo Abrahamu
anayandikira nati, Kodi mudzaononga olungama pamodzi ndi oipa? 24Kapena
alipo olungama makumi asanu m'kati mwa mudzi; kodi mudzaononga,
simudzasiya malowa cifukwa ca olungama makumi asanu ali
momwemo? 25Musamatero ai, kupha olungama pamodzi ndi oipa, kuta
olungama akhale monga oipa; musamatero ai; kodi sadzacita zoyenera

woweruza wa dziko lonse lapansi? 26Ndipo anati Yehova, Ndikapeza m'Sodomu olungama makumi asanu m'kati mwa mudzi, ndidzasiya malo onse cifukwa ca iwo. 27Ndipo anayankha Abrahamu nati, Taonanitu, ndadziyesera kunena kwa Ambuye, ine ndine pfumbi ndi phulusa: 28kapena akaperewera asanu pa olungama makumi asanuwo; kodi mudzaononga mudzi wonse cifukwa ca kuperewera asanu? Ndipo anati, Ndikapeza makumi anai ndi asanu sindidzauononga. 29Ndipo ananenanso kwa iye nati, Kapena akapezedwa makumi anai m'menemo. Ndipo anati, Sindidzacita cifukwa ca makumi anai. 30Ndipo anati, Asakwiyetu Ambuye, ndipo ndidzanenanso: kapena akapezedwa makumi atatu m'menemo? Ndipo anati, Ndikapeza makumi atatu m'menemo sindidzacita. 31Ndipo anati, Taonanitu, ndadziyesera kunena kwa Ambuye: kapena akapezedwa makumi awiri m'menemo. Ndipo anati, Sindidzacita cifukwa ca makumi awiri. 32Ndipo anati, Asakwiyetu Ambuye, ndipo ndidzanena kamodzi aka kokha: kapena akapezedwakhumim'menemo: Ndipo anati, Sindidzacita cifukwa ca khumi. 33Ndipo Yehova anapita atatha kunena naye Abrahamu: ndipo Abrahamu anabwera kumalo kwace.

Genesis 19

Cionongeko ca Sodomu ndi Gomora

1Ndipo anadza ku Sodomu madzulo amithenga awiri; ndipo Loti anakhala pa
cipata ca Sodomu, ndipo Loti anaona iwo, nauka kuti akakomane nao, ndipo
anaweramitsa pansi nkhope yace. 2Ndipo anati, Taonanitu, ambuye anga,
tembenukanitu, kulowa m'nyumba mwa kapolo wanu, mugone usiku wonse,
mutsuke mapazi anu, ndipo mudzalawira m'mawa kunka ulendo wanu. Ndipo
anati, lai; koma tigone m'khwalalamu usiku wonse. 3Ndipo anawaumiriza iwo
ndithu: ndipo anapatukira kwa iye, nalowa m'nyumba mwace; ndipo
anawakonzera iwo madyerero, naphika mikate yopanda cotupitsa, ndipo
anadya, 4Koma asanagone, anthu a m'mudzimo anthu a Sodomu, anazinga
nyumba, anyamata ndi okalamba, anthu onse a m'mbali zonse; 5ndipo
anamuitana Loti, nati kwa iye, Ali kuti anthu amene anadza kwa iwe madzulo
ano, utiturutsire iwo kuti tiwadziwe. 6Ndipo Loti anaturukira kwa iwo pakhomo,
natseka cambuyo pakhomo pace. 7Ndipo anati, Abale anga, musacitetu koipa
kotere. 8Taonanitu, ndiri ndi ana akazi awiri, amene sanadziwe mwamuna;
ndiwaturutsire iwo kwa inu, mucite nao comwe cikomera inu; koma anthu awa
musawacitire iwo kanthu; cifukwa kuti anadza iwo pansi pa mthunzi wa cindwi
langa, 9Ndipo anati iwo, Baima; natinso, Uyu anadza kuno kukhala ngati
mlendo, ndipo afuna kutilamulira; tsopano tidzakucitira iwe koipa koposa iwo.
Ndipo iwo anamkakamiza munthuyo Loti ndithu, nayandikira kuti aswe
citseko. 10Komo anthu aja anaturutsa dzanja lao, namlowetsa Loti momwe
anali iwo m'nyumba, natseka pakhomo, 11Ndipo anacititsa khungu m'maso
mwa anthu amene anali pakhomo pa nyumba, ang'ono ndi akuru, ndipo
anabvutika kufufuza pakhomo. 12Ndipo anthu aja anati kwa Loti, Kodi muli nao
ena pano? Mkamwini, ndi ana ako amuna, ndi ana ako akazi, ndi onse ali nao
m'mudzi muno, uturuke nao m'malo muno: 13popeza ife tidzaononga malo ano,
cifukwa kulira kwao kwakula pamaso pa Yehova, ndipo Yehova anatitumiza ife
kuti tiuononge. 14Ndipo anaturuka Loti nanena nao akamwini ace amene
anakwata ana ace akazi, nati, Taukani, turukani m'malo muno; popeza Yehova
adzaononga mudziwu; koma akamwini ace anamyesa wongoseka. 15Pamene
kunaca, amithengawo anafulumiza Loti, nati, Uka, tenga mkazi wako, ndi ana
ako akazi awiri amene ali kunowa, kuti munganyeke m'mphulupulu ya
mudzi. 16Koma anacedwa; ndipo anthuwo anamgwira dzanja lace, ndi dzanja
la mkazi wace ndi dzanja la ana ace akazi awiri; cifukwa ca kumcitira cifundo
Yehova; ndipo anamturutsa iye, namuika kunja kwa mudzi. 17Ndipo panali
pamene anawaturutsa iwo kunja, anati, Tapulumuka ndi moyo wako; usaceuke,
usakhale pacigwa pali ponse; thawira kuphiri, kuti unganyeke. 18Ndipo Loti
anati kwa iwo, Iaitu, mfumu; 19taonanitu, kapolo wanu anapeza ufulu pamaso
panu, ndipo munakuza cifundo canu, cimene munandicitira ine, pakupulumutsa
moyo wanga; ine sindikhoza kuthawira kuphiri kuti cingandipeze ine coipaco
ndingafe: 20taonanitu, mudzi uwu uli pafupi pothawirapo, ndipo uli wong'ono;
ndithawiretu kumeneko, suli wong'ono nanga? ndipo ndidzakhala ndi
moyo. 21Ndipo anati kwa iye, Taona, ndikubvomereza iwe pamenepanso kuti
sindidzaononga mudzi uwu umene wandiuza. 22Fulumira, thawira kumeneko;
pakuti sindithai kucita kanthu usadafike kumeneko. Cifukwa cace anacha dzina
la mudziwo Zoari. 23Ndipo dzuwa lidakwera pa dziko pamene Loti anafika ku

Zoari. 24Ndipo Yehova anabvumbitsa pa Sodomu ndi pa Gomora miyala ya
sulfure ndi mota kuturuka kwa Mulungu kumwamba; 25ndipo anaononga
midziyo, ndi cigwa conse, ndi onse akukhala m'midzimo, ndi zimene zimera
panthaka. 26Koma mkazi wace anaceuka ali pambuyo pace pa Loti, nasanduka
mwala wamcere. 27Ndipo Abrahamu analawiram'mamawa kunka kumalo
kumene anaima pamaso pa Yehova: 28ndipo anayang'anira ku Sodomu ndi ku
Gomora ndi ku dziko lonse la cigwa, ndipo anapenya, taonanitu, utsi wa dzikolo
unakwera, monga utsi wa ng'anjo.
29Ndipo panali pamene Mulungu anaononga midzi ya m'cigwa, Mulungu
anakumbukira Abrahamu, naturutsa Loti pakati pa cionongeko, pamene
anaononga midzi m'mene anakhalamo Loti.

Gwero La Amon; ndi Moabu

30Ndipo Loti anabwera kuturuka m'Zoari nakhala m'phiri ndi ana akazi awiri
pamodzi naye: cifukwa anaopa kukhala m'Zoari, ndipo anakhata m'phanga, iye
ndi ana ace akazi. 31Woyamba ndipo anati kwa wamng'ono, Atate wathu
akalamba, ndipo palibe pa dziko lapansi mwamona amene adzalowa kwa ife
monga amacita pa dziko lonse lapansi: 32tiyeni, timwetse atate vinyo,
tidzagona naye, kuti tisunge mbeu za atate wathu. 33Ndipo anamwetsa atate
wao vinyo usiku womwewo; woyamba ndipo analowa nagona naye atate wace;
ndipo sanadziwa pomwe anagona ndi pomwe anauka, 34Ndipo panali
m'mamawa, woyamba anati kwa wamng'ono, Taona, ndinagona ine ndi atate
wanga usiku walero: timwetsenso iye usikunso: udzalowe nugone naye kuti
tisunge mbeu za atate wathu. 35Ndipo anamwetsa vinyo atate wao usiku
womwenso; wamng'ono ndipo anauka nagona naye; ndipo iye sanadziwa
pomwe anagona ndi pomwe anauka. 36Ndipo ana akazi awiri a Loti anali ndi
pakati pa atate wao. 37Woyamba ndipo anabala mwana wamwamona, namcha
dzina lace. Moabu; yemweyo ndi atate wa Amoabu kufikira lero. 38Wamng'ono
ndipo anabala mwana wamwamuna, namcha dzina lace Benammi; yemweyo
ndi atate wa Aamoni kufikira lero.

Genesis 20

Abrahamu kwa mfumu Abimeleke

1Abrahamu ndipo anacoka kumeneko kunka ku dziko la kumwera, ndipo
anakhala pakati pa Kedesi ndi Suri, ndipo anakhala ngati mlendo
m'Gerari. 2Ndipo Abrahamu anati za Sara mkazi wace, Iye ndiye mlongo
wanga: ndipo Abimeleke mfumu ya Gerari anatumiza namtenga Sara. 3Koma
Mulungu anadza kwa Abimeleke m'kulota kwa usiku, nati kwa iye, Taona,
wakufa iwe, cifukwa ca mkazi amene wamtenga: pakuti iye ndiye mkazi wa
mwini. 4Koma Abimeleke sanayandikire naye; ndipo anati, Ambuye, kodi
mudzaphanso mtundu wolungama? 5Kodi iye sanati kwa ine, Ndiye mlongo
wanga: ndipo mkazi iye yekha anati, iye ndiye mlongo wanga: ndi mtima wanga
wangwiro ndi manja anga osacimwa ndacita ine ici. 6Ndipo Mulungu anati kwa
iye m'kulota, lode ndidziwa ine, kuti wacita ico ndi mtima wangwiro, ndipo
lnenso ndinakuletsa iwe kuti usandicimwire ine: cifukwa cace sindinakuloleza
iwe kuti umkhudze mkaziyo. 7Tsopano, umbwezere munthuyo mkazi wace;
cifukwa iye ndiye mneneri, ndipo adzakupempherera iwe, ndipo udzakhala ndi
moyo: koma ukaleka kumbwezera, udziwe kuti udzafa ndithu, iwe ndi onse
amene uli nao. 8Ndipo Abimeleke analawira m'mamawa, naitana anyamata ace
onse, nanena zonse rimenezo m'makutu mwao, ndipo anthu anaopa
kwambiri. 9Ndipo Abimeleke anaitana Abrahamu, nati kwa iye, Waticitira ife
ciani iwe? Ndakucimwiranji iwe kuti waufikitsa pa ine ndi pa ufumu wanga
ucimo waukuru? Wandicitira ine zosayenera kuzicita. 10Ndipo Abimeleke anati
kwa Abrahamu, Unaona ciani iwe kuti wacita ici? 11Ndipo Abrahamu anati,
Cifukwa ndinati, Pompano palibe ndithu kumuopa Mulungu, ndipo adzandipha
ine cifukwa ca mkazi wanga. 12Koma ndiye mlongo wanga ndithu, mwana wa
atate wanga, koma si mwana wa amai wanga: ndipo anakhala ndi ine mkazi
wanga. 13Ndipo panali pamene Mulungu anandiyendetsa ine kunyumba kwa
atate wanga, ndinati kwa mkaziyo, Ici ndico cokoma mtima udzandicitire ine,
konse kumene tidzafika ife, uzinena za ine, iye ndiye mlongo wanga. 14Ndipo
Abimeleke anatenga nkhosa ndi ng'ombe nd akapolo ndi adzakazi nampatsa
Abrahamu, nambwezera iye Sara mkazi wace. 15Ndipo Abimeleke anati, Taona
dziko langa liri pamaso pako; kumene kuli kwabwino pamaso pako takhala
kumeneko. 16Kwa Sara ndipo anati, Taona, ndapatsa mlongo wako ndalama za
siliva mazana khumi; taona, izo ndizo zoyeretsa maso za kwa onse amene ali
ndi iwe: ndi pamaso pa onse ukhale wolungama. 17Ndipo Abrahamu
anapemphera Mulungu, ndipo Mulungu anaciritsa Abimeleke, ndi mkazi wace,
ndi adzakazi ace; ndipo anabala ana. 18Pakuti Yehova anatseketsa mimba
yonse ya a m'nyumba ya Abimeleke, cifukwa ca Sara mkazi wace wa
Abrahamu.

Genesis 21

Kubadwa kwa Isake

1Ndipo Yehova anayang'anira Sara monga momwe anati, ndipo Yehova
anamcitira iye monga ananena. 2Ndipo Sara anatenga pakati, nambalira
Abrahamu m'ukalamba wace mwana wamwamuna, nthawi yomweyo Mulungu
anamuuza iye. 3Ndipo Abrahamu anamucha dzina lace la mwana wace
wamwamuna amene anabala iye, amene anambalira iye Sara, Isake. 4Ndipo
Abrahamu anamdula mwana wace wamwamuna Isake pamene anali wa
masiku ace asanu ndi atatu, monga Mulungu anamlamulira iye. 5Ndipo
Abrahamu anali wa zaka zana limodzi pamene anambadwira iye Isake mwana
wace. 6Ndipo Sara anati, Mulungu anandisekeretsa ine; onse akumva
adzasekera pamodzi ndi ine. 7Ndipo anati, Akadatero ndani kwa Abrahamu kuti
Sara adzayamwitsa ana? pakuti ndambalira iye mwana wamwamuna
m'ukalamba wace.

Abrahamu acotsa Hagara

8Ndipo anakula mwanayo naletsedwa kuyamwa: ndipo Abrahamu anakonza
madyerero akuru tsiku lomwe analetsedwa Isake kuyamwa. 9Ndipo Sara
anaona mwana wace wamwamuna wa Hagara M-aigupto, amene anambalira
Abrahamu, alinkuseka. 10Cifukwa cace anati kwa Abrahamu, Cotsa mdzakazi
uyo, ndi mwana wace wamwamuna; cifukwa mwana wa mdzakazi uyo
sadzalowa m'nyumba pamodzi naye mwana wanga Isake. 11Ndipo mauwo
anaipira Abrahamu cifukwa ca mwana wace. 12Ndipo Mulungu anati kwa
Abrahamu, Usaipidwe nao, cifukwa ca mnyamatayo, ndi cifukwa ca mdzakazi
wako; momwe monse akunenera iwe Sara umvere iwe mau ace; cifukwa kuti
mwa Isake zidzaitanidwa mbeu zako. 13Ndipo mwana wamwamuna wa
mdzakazi uyo ndidzayesa mtundu, cifukwa iye ndiye mbeu yako. 14Ndipo
Abrahamu analawira m'mamawa, natenga mkate ndi mcenje wa madzi,
nampatsa Hagara, naika paphewa pace, ndi mwana, namcotsa iye: ndipo iye
anamuka, nasocerera m'cipululu ca Beereseba. 15Ndipo anatha madzi a
m'mcenje ndipo anaika mwana pansi pa citsamba. 16Ndipo ananka nakhala
pansi popenyana naye patari, monga pakugwa mubvi: cifukwa anati, Ndisaone
kufa kwa mwana. Ndipo anakhala popenyana naye, nakweza mau ace
nalira, 17Ndipo Mulungu anamva mau a mnyamatayo, ndi mthenga wa
Mulungu anamuitana Hagara, ndi mau odzera kumwamba, nati kwa iye, Watani
Hagara? usaope; cifukwa Mulungu anamva mau a mnyamata kumene
ali. 18Tauka, nuukitse mnyamatayo, ndi kumgwira m'dzanja lako; cifukwa
ndidzamuyesa iye mtundu waukuru. 19Ndipo Mulungu anamtsegula m'maso
mwace, ndipo anaona citsime ca madzi; namuka nadzaza mcenje ndi madzi,
nampatsa mnyamata kuti amwe. 20Ndipo Mulungu anakhala ndi mnyamata,
ndipo anakula iye; nakhala m'cipululu, nakhala wauta. 21Ndipo anakhala
m'cipululu ca Parana; ndipo amace anamtengera iye mkazi wa ku dziko la
Aigupto.

Abrahamu apangana ndi Abimeleke

22Ndipo panali nthawi yomweyo. Abimeleke ndi Fikolo kazembe wa nkhondo
yace anati kwa Abrahamu, kuti, Mulungu ali pamodzi ndi iwe m'zonse uzicita
iwe; 23tsopano iwe undilumbirire ine pano pa Mulungu kuti sudzandinyenga ine,
kapena mwana wanga, kapena mdzukulu wanga: koma monga ufulu

ndakucitira iwe udzandicitire ine, ndi dziko lomwe wakhalamo, ngati mlendo. 24Ndipo Abrahamu anati, Ine ndidzalumbira. 25Ndipo Abrahamu anamdzudzula Abimeleke cifukwa ca citsime ca madzi, anyamata ace a Abimeleke anacilanda. 26Ndipo anati Abimeleke, Sindinadziwe amene anacita ico; ndipo iwe sunandiuze ine, ndiponso sindinamve koma lero lino. 27Ndipo Abrahamu anatenga nkhosa ndi ng'ombe, nampatsa Abimeleke, ndipo anapangana pangano onse awiriwo. 28Ndipo Abrahamu anapatula ana a nkhosa akazi asanu ndi awiri pa okha. 29Ndipo Abimeleke anati kwa Abrahamu, Nanga ana a nkhosa akazi asanu ndi awiri amene wapatula pa okha? 30Ndipo anati, Ana a nkhosa akazi asanu ndi awiriwa uwalandire pa dzanja langa, kuti akhale mboni zanga, kuti ndakumba ine citsime cimeneci. 31Cifukwa cace anacha malowo Beereseba: cifukwa pamenepo analumbira onse awiri. 32Ndipo anapangana pangano pa Beereseba: ndipo anauka Abimeleke ndi Fikolo kazembe wa-nkhondo yace, nabwera kunka ku dziko la Afilisti. 33Ndipo Abrahamu ananka mtengo wabwemba pa Beereseba, naitanira pamenepo dzina la Yehova, Mulungu wa nthawi zonse. 34Ndipo Abrahamu anakhala ngati mlendo masiku ambiri m'dziko la Afilisti.

Genesis 22

Isake aperekedwa nsembe

1Ndipo panali zitapita zimenezo, Mulungu anamuyesa Abrahamu nati kwa iye, Abrahamu; ndipo anati, Ndine pano. 2Ndipo anati, Tengatu mwana wako, wamwamuna wayekhayo, Isake, amene ukondana naye, numuke ku dziko la Moriya; numpereke iye kumeneko nsembe yopsereza pa limodzi la mapiri lomwe ndidzakuuza iwe. 3Ndipo Abrahamu analawira m'mamawa namanga buru wace, natengako anyamata ace awiri pamodzi naye, ndi Isake mwana wace, nawaza nkhuni za nsembe, nauka, nanka kumalo komwe Mulungu anamuuza iye, 4Tsiku lacitatu Abrahamu anatukula maso ace naona malowo patari. 5Ndipo Abrahamu anati kwa anyamata ace, Khalani kuno ndi buru, ine ndi mwanayu tinka uko, ndipo tikapemphera ndi kubweranso kwa inu. 6Ndipo Abrahamu anatenga nkhuni za nsembe yopsereza, nazisenzetsa Isake mwana wace; natenga mota m'dzanja lace ndi mpeni; nayenda pamodzi onse awiri. 7Ndipo Isake ananena ndi Abrahamu atate wace, nati, Atate wanga; ndipo iye anati, Ndine pano, mwana wanga. Ndipo anati, Taonani moto ndi nkhuni; koma mwana wa nkhosa wa nsembe yopsereza ali kuti? 8Ndipo Abrahamu anati, Mwana wanga, Mulungu adzadzifunira yekha mwana wa nkhosa wa nsembe yopsereza; nayenda pamodzi onse awiri. 9Ndipo anafika kumalo komwe Mulungu anamuuza iye; ndipo Abrahamu anamanga guwa la nsembe nakonza nkhuni, namanga Isake mwana wace, namuika iye pa guwa la nsembe pamwamba pa nkhuni. 10Ndipo Abrahamu anatambasula dzanja lace, natenga mpeni kuti amuphe mwana wace. 11Koma mthenga wa Yehova anamuitana iye ndi mau odzera kumwamba, nati, Abrahamu, Abrahamu; ndi iye anati, Ndine pano. 12Ndipo mthenga anati, Usaike dzanja lako pa mwana, usamcitire iye kanthu; cifukwa tsopano ndidziwa kuti iwe umuopa Mulungu, pakuti sunandikanize ine mwana wako, mwana wako wayekha. 13Ndipo Abrahamu anatukula maso ace nayang'ana taonani, pambuyo pace nkhosa yamphongo yogwiridwa ndi nyanga zace m'ciyangoyangomo; ndipo ananka Abrahamu nakatenga nkhosa yamphongoyo, naipereka nsembe yopsereza m'malo mwa mwana wace. 14Ndipo Abrahamu anacha dzina lace la malowo Yehova-Yire: monga ati lero lomwe, M'phiri la Yehova cidzaoneka. 15Ndipo mthenga wa Yehova anamuitana Abrahamu ndi mau odzera kumwamba kaciwiri, 16nati, Pa Ine ndekha ndalumbira, ati Yehova, popeza wadta ici, sunandikaniza mwana wako, mwana wako wa yekha, 17kudalitsa ndidzakudalitsa iwe, kucurukitsa ndidzacurukitsa mbeu zako monga nyenyezi za kumwamba, monga mcenga wa m'mphepete mwa nyanja; ndipo mbeu zako zidzagonjetsa cipata ca adani ao; 18m'mbeu zako mitundu yonse ya dziko lap ansi idzadalitsidwa: cifukwa wamvera mau anga. 19Ndipo Abrahamu anabwera kwa anyamata ace, ndipo anauka nayenda pamodzi kumuka ku Beereseba; ndipo anakhala Abrahamu pa Beereseba.

20Ndipo panali zitapita izi, anauza Abrahamu kuti, Taonani, Milika iyenso anambalira Nahori mphwako ana; 21Huzi woyamba ndi Buzi mphwace, ndi Kemueli atate wace wa Aramu; 22ndi Kesede, ndi Hazo, ndi Pilidasi ndi Yidilafi, ndi Betuele. 23Ndimo Betuele anabala Rebeka: amenewa asanu ndi atatu Milika anambalira Nahori mphwace wa Abrahamu. 24Ndipo mkazi wace

wamng'ono, dzina lace Rcuma, iyenso anabala Teba, ndi Gahamu, ndi Tahasi, ndi Maaka.

Genesis 23

Imfa ndi kuikidwa kwa Sara

1Ndipo Sara anali wa zaka zana limodzi kudza makumi awiri ndi zisanu ndi
ziwiri: ndizo zaka za moyo wa Sara. 2Ndipo Sara anafa m'Kiriyati-araba (ndiwo
Hebroni), m'dziko la Kanani; ndipo Abrahamu anadza ku maliro a Sara, kuti
amlire. 3Ndipo Abrahamu anauka pa wakufa wace, nanena kwa ana a Heti,
nati, 4Ine ndine mlendo wakukhala ndi inu: mundipatse ndikhale ndi manda
pamodzi ndi inu, kuti ndiike wakufa wanga ndisamthirenso maso. 5Ndipo ana a
Heti anayankha Abrahamu nati kwa iye, 6Mutimvere ife mfumu, ndinu karonga
wamkuru pakati pa ife; muike wakufa wanu m'manda mwathu mosankhika:
palibe munthu yense wa ife adzakaniza manda ace, kuti muike wakufa
wanu. 7Ndipo anauka Abrahamu naweramira anthu a m'dzikomo, ana a
Heti. 8Ndipo ananena nao, kuti, Ngati mukandibvomereza kuti ndiike wakufa
wanga ndisamthirenso maso, mundimvere ine, mundinenere ine kwa Efroni
mwana wace wa Zohari, 9kuti andipatse ine phanga la Makipela, limene liri
pansonga pa munda wace; pa mtengo wace wonse andipatse pakati pa inu,
ndikhale nao manda. 10Ndipo Efroni anakhala pakati pa ana a Heti: ndipo
Efroni Mhiti anayankha Abrahamu alinkumva ana a Heti, onse amene analowa
pa cipata ca mudzi wace, kuti, 11Iai, mfumu, mundimvere ine; munda
ndikupatsani inu, ndi phanga liri m'menemo ndikupatsani inu, pamaso pa ana a
anthu anga ndikupatsani inu; ikani wakufa wanu. 12Ndipo Abrahamu
anawerama pamaso pa anthu a m'dzikomo. 13Ndipo ananena kwa Efroni
alinkumva anthu a m'dzikomo, kuti, Koma ngati ufuna, undimveretu ine:
ndidzakupatsa iwe mtengo wace wa munda; uulandire kwa ine, ndipo ndidzaika
wakufa wanga m'menemo. 14Ndipo Efroni anamyankha Abrahamu, nati kwa
iye, 15Mfumu, mundimvere ine; kadziko ka mtengo wace wa masekele a siliva
mazana anai, ndiko ciani pakati pa ine ndi inu? ikani wakufa wanu. 16Ndipo
Abrahamu anamvera Effoni, ndipo Abrahamu anamuyesera Efroni ndalama
zimene ananena alinkumva ana a Heti, masekele a siliva mazana anai,
ndalama zomwezo agulana nazo malonda. 17Ndipo munda wa Efroni umene
unali m'Makipela, umene unali patsogolo pa Mamre, munda ndi phanga liri
momwemo, ndi mitengo yonse inali m'mundamo, yokhala m'malire monse
mozungulira momwemo, 18inalimbitsidwa kwa Abrahamu ikhale yace, pamaso
pa ana a Heti, pa onse amene analowa pa cipata ca mudzi wace. 19Zitatha izi
Abrahamu anaika Sara mkazi wace m'phanga la munda wa Makipela patsogolo
pa Mamre (ndiwo Hebroni), m'dziko la Kanani. 20Ndipo ana a Heti analimbitsira
Abrahamu munda, ndi phanga liri m'menemo, likhale lace lamanda.

Genesis 24

Rebeka apalidwa ubwenzi ndi Isake

1Ndipo Abrahamu anali wokalamba, nagonera zaka zambiri; ndipo Yehova
anadalitsa Abrahamu m'zinthu zonse. 2Ndipo Abrahamu anati kwa mnyamata
wace wamkuru wa pa nyumba yace, amene analamulira pa zonse anali nazo,
Taikatu dzanja lako pansi pa ncafu yanga: 3ndipo ndidzakulumbiritsa iwe pa
Yehova, Mulungu wa Kumwamba, ndi Mulungu wa dziko lapansi, kuti
usadzamtengere mwana wanga mkazi wa kwa ana akazi a Akananiwo, amene
ndikhala pakati pao. 4Koma udzanke ku dziko langa, kwa abale anga, ndi
kumtengera mwana wanga Isake mkazi. 5Ndipo anati kwa iye mnyamatayo,
Kapena sadzafuna mkaziyo kunditsata ine ku dziko lino: kodi
ndikambwezerenso mwana wanu kudziko komwe mwacokera inu? 6Ndipo
Abrahamu anati kwa iye, Cenjera iwe, usambwezerenso mwana wanga
kumeneko. 7Yehova Mulungu wa Kumwamba, amene ananditenga ine ku
nyumba ya atate wanga, ku dziko la abale anga, amene ananena ndi ine,
amene analumbirira ine kuti, Ndidzapatsa mbeu zako dziko ili; iye adzatumiza
mthenga wace akutsogolere, ndipo udzamtengere mwana wanga mkazi
kumeneko. 8Ndipo ngati sadzafuna mkaziyo kukutsata iwe, udzakhala
wosacimwa pa cilumbiro cangaci: koma mwana wanga usambwezerenso
kumeneko. 9Ndipo mnyamatayo anaika dzanja lace pansi pa ncafu yace ya
Abrahamu mbuye wace, namlumbirira iye za cinthuco. 10Ndipo mnyamatayo
anatenga ngamila khumi za mbuyace, namuka: cifukwa kuti cuma conse ca
mbuyace cinali m'dzanja lace: ndipo anacoka namuka ku Mesopotamiya, ku
mudzi wa Nahori. 11Ndipo anagwaditsa ngamila zace kunja kwa mudzi, ku
citsime ca madzi nthawi yamadzulo, nthawi yoturuka akazi kudzatunga
madzi. 12Ndipo anati, Yehova, Mulungu wa mbuyanga Abrahamu
mundiyendetse ine bwino lero lino, mumcitire ufulu mbuyanga
Abrahamu, 13Taonani, ine ndiima pa citsime ca madzi; ndipo ana akazi a
m'mudzi aturuka kudzatunga madzi; 14ndipo pakhale kuti namwali amene
ndidzati kwa iye, Tulatu mtsuko wako, ndimwe; ndipo iye adzati, Imwa, ndipo
ndidzamwetsanso ngamila zako; yemweyo akhale mkazi wosankhira mnyamata
wanu Isake; ndipo cotero ndidzadziwa kuti mwamcitira mbuyanga
ufulu. 15Ndipo panali, asanathe kunena, taonani, anaturuka Rebeka, amene
anambala Betuele, mwana wamwamuna wa Milika, mkazi wa Nahori mphwace
wa Abrahamu, ndi mtsuko wace paphewa pace. 16Ndipo namwaliyo anali
wokongola kwambiri m'maonekedwe ace, ndiye namwali wosamdziwa
mwamuna, ndipo anatsikira kukasupe, nadzaza mtsuko wace,
nakwera. 17Ndipo mnyamatayo anamthamangira kukomana naye, nati,
Ndimwetu madzi pang'ono a m'mtsuko mwako. 18Ndipo anati, Imwa
mbuyanga; nafulumira nayangata mtsuko m'manja mwace namwetsa
iye. 19Atatha kumwetsa iye, anati, Ndidzatungiranso ngamila zako, mpaka
zitamwa zonse. 20Ndipo anafulumira nathira madzi a m'mtsuko wace
m'comwera, nathamangiranso kucitsime kukatunga, nazitungira ngamila zace
zonse. 21Munthuyo ndipo anamyang'anira iye, nakhala cete, kuti adziwe ngati
Yehova anamuyendetsa bwino kapena iai. 22Ndipo panali zitatha kumwa
ngamila, munthuyo anatenga mphete yagolidi ya kulemera kwace sekele
latheka, ndi zingwinjiri ziwiri za m'manja ace, kulemera kwace masekele khumi

a golidi. 23Ndipo anati, Ndiwe mwana wa yani? Undiuzetu. Kodi ku nyumba ya atate wako kuli malo akuti tigoneko ife? 24Ndipo mkaziyo anati kwa iye, Ine ndine mwana wa Betuele mwana wamwamuna wa Milika, amene anambalira Nahori. 25Natinso kwa iye, Tiri nao maudzu ndi zakudya zambiri oeli malo ogona. 26Munthuyo oelipo anawerama mutu namyamika Yehova. 27Ndipo anati, Ayamikike Yehova Mulungu wa mbuyanga Abrahamuamene sanasiya mbuyanga wopanda cifundo cace ndi zoona zace: koma ine Yehova Wanditsogolera m'njira ya ku nyumba ya abale ace a mbuyanga. 28Namwaliyo ndipo anathamanga nawauza zimenezo ku nyumba ya amace. 29Ndipo Rebeka anali ndi mlongo wace dzina lace Labani; ndipo Labani anathamangira munthuyo kunja ku kasupe. 30Ndipo panali, pamene anaona mphete ndi zingwinjiri pa manja a mlongo wace, pamene anamva mau a Rebeka mlongo wace, akuti, Cotero ananena ndi ine munthuyo; Labani anafika pa munthuyo; taonani, anaimirira pa ngamila pakasupe. 31Ndipo anati, Talowa iwe, wodalitsidwa ndi Yehova; uimiriranji kunjako? cifukwa kuti ndakonzeratu nyumba, ndi malo a ngamila. 32Munthuyo ndipo analowa m'nyumba, namasula ngamila, napatsa ngamila maudzu ndi cakudya, ndi madzi akusamba mapazi ace ndi mapazi a iwo amene anali naye. 33Ndipo anaika cakudya pamaso pace: koma anati, Sindidzadya ndisananene cimene ndadzera. Ndipo anati, Nenatu. 34Ndipo anati, Ine ndine mnyamata wa Abrahamu. 35Yehova wamdalitsa mbuyanga kwambiri; ndipo anakula kwakukuru; ndipo anampatsa iye nkhosa ndi ng'ombe, ndi siliva ndi golidi, ndi akapolo ndi adzakazi, oeli ngamila ndi aburu. 36Ndipo Sara mkazi wace wa mbuyanga anambalira mbuyanga mwana wamwamuna, mkaziyo anali wokalamba; ndipo anampatsa mwanayo zonse ali nazo. 37Ndipo mbuyanga anandilumbiritsa ine kuti, Usamteogere mwana wanga mkazi wa ana akazi a Kanani, m'dziko mwao m'mene ndikhala ine; 38koma udzanke ku nyumba ya atate wanga, kwa abale anga, ndi kumtengera mwana wanga mkazi. 39Ndipo ndinati kwa mbuyanga, Kapena mkazi sadzanelitsata ine. 40Ndipo anati kwa ine, Yehova, amene ndiyenda ine pamaso pace, adzatumiza mthenga wace pamodzi ndi iwe, nadzakuyendetsa bwino m'njira yako; ndipo ukamteogere mwana wanga mkazi wa mwa abale anga ndi ku nyumba ya atate wanga; 41ukatero udzakhala wosacimwa pa malumbiro ako, pofika iwe kwa abate anga; ndipo ngati sadzakupatsa iwe, udzakhala wosacimwa pa malumbiro ako. 42Ndipo ndinafika lero kukasupe, ndipo ndinati, Yehova Mulungu wa mbuyanga Abrahamu, ngati mundiyendetsatu bwino njira yanga m'mene ndinkamo ine; 43taonani, ine ndiima pa kasupe wa madzi, ndipo pakhale, kuti namwali amene aturuka kudzatunga madzi, ndikati kwa iye, Ndipatse madzi ndimwe pang'ono m'mtsuko mwako; 44ndipo iye akati kwa ine, Imwatu iwe, ndiponso ndidzatungira ngamila zako; yemweyo akhale mkazi amene Yehova wamsankhira mwana wa mbuyanga. 45Ndisanathe kunena m'mtima mwanga, taonani, Rebeka anaturuka ndi mtsuko wace pa phewa lace, natsikira kukasupe, natunga: ndipo ndinati kwa iye, Ndimwetu. 46Ndipo iye anafulumira, natsitsa mtsuko pa phewa lace, nati, Imwatu, ndipo ndidzamwetsanso ngamila zako: ndipo ndinamwa, ndipo anamwetsa ngamila. 47Ndipo ndinamfunsa iye kuti, Ndiwe mwana wa yani kodi? Ndipo anati, Ndine mwana wa Betuele, mwana wa Nahori amene

anambalira iye Milika: ndipo ndinaika mphete pamphuno pace ndi zingwinjiri pa manja ace. 48Ndipo ndinawerama mutu wanga ndi kulambira Yehova, ndi kumyamikira Yehova, Mulungu wa mbuyanga Abrahamu, amene ananditsogolera ine m'njira yakuona, kuti ndikamtengere mwana wamwamuna wace mwana wamkazi wa mphwace wa mbuyanga. 49Tsopano, ngati mudzamcitira mbuyanga zaufulu ndi zoonadi, mundiuze, ngati iai, mundiuze; kuti ndipatukire ku dzanja lamanja kapena ku dzanja lamanzere. 50Ndipo anayankha Labani ndi Betuele, nati, Caturuka kwa Yehova cinthu ici; sitingathe kunena ndi iwe coipa kapena cabwino. 51Taonani, Rebeka ali pamaso pako, mtenge ndi kumuka, akhale mkazi wa mwana wa mbuyako, monga wanena Yehova. 52Ndipo panali pamene anamva mauwo mnyamata wa Abrahamu, anamgwadira Yehova pansi, 53Ndipo mnyamatayo anaturutsa zokometsera zasiliva ndi zokometsera zagolidi, ndi zobvala, nampatsa Rebeka: ndipo anapatsa za mtengo wapatari kwa mlongo wace ndi amace. 54Ndipo anadya namwa iye ndi anthu amene anali pamodzi naye, nagonapo usiku: ndipo anauka m'mamawa, ndipo iye anati, Mundilole ine ndinke kwa mbuyanga. 55Ndipo mlongo wace ndi amace anati, Namwali akhale ndi ife masiku akuwerengeka, afikire khumi; patsogolo pace iye adzamuka. 56Ndipo iye anati kwa iwo, Musandicedwetse ine, pakuti Yehova wandiyendetsa bwino m'njira yanga: mundilole ine ndinke kwa mbuyanga. 57Ndipo anati iwo, Tidzamuitana namwaliyo, tidzamfunsa pakamwa pace. 58Ndipo anamuitana Rebeka nati kwa iye, Kodi udzanka pamodzi ndi munthuyo? Ndipo anati, Ndidzanka. 59Ndipo anamlola Rebeka mlongo wao ndi mlezi wace, amuke pamodzi ndi mnyamata wace wa Abrahamu, ndi anthu ace. 60Ndipo anamdalitsa Rebeka, nati kwa iye, Mlongo wathu ndiwe, iwe ukhale amai wa anthu zikwizikwi, mbeu zako zigonjetse cipata ca iwo akudana nao. 61Ndipo adauka Rebeka ndi anamwali ace, nakwera pa ngamila natsata munthuyo: mnyamatayo ndipo anamtenga Rebeka namuka. 62Ndipo Isake anadzera njira ya Beereahai-roi; cifukwa kuti anakhala iye n'dziko la kumwera. 63Ndipo Isake anaturuka kulingalira m'munda madzulo; ndipo anatukula maso ace, nayang'ana, taona, ngamila zinalinkudza, 64Ndipo Rebeka anatukula maso ace, ndipo pamene anaonalsake anatsika pa ngamila, 65Ndipo anati kwa mnyamata, Munthuyo ndani amene ayenda m'munda kukomana ndi ife? Mnyamatayo ndipo anati, Uyo ndi mbuyanga: cifukwa cace namwali anatenga cophimba cace nadziphimba. 66Mnyamatayo ndipo anamuuza Isake zonse anazicita. 67Ndipo Isake anamlowetsa mkaziyo m'hema wa amace Sara, namtenga Rebeka, nakhala iye mkazi wace; ndipo anamkonda iye; ndipo Isake anatonthozedwa mtima atafa amace.

Genesis 25

Kumwalira kwa Abrahamu

1Ndipo Abrahamu anatenga mkazi wina dzina lace Ketura. 2Ndipo anambalira
iye Zimerani ndi Yokesani ndi Medani, ndi Midyani, ndi Yisebaki, ndi
Sua. 3Ndipo Yokesani anabala Seba, ndi Dedani. Ana a Dedani ndi Aasuri, ndi
Aletusi, ndi Aleumi. 4Ana a Midyani: Efa, ndi Efere, ndi Hanoki, ndi Abida, ndi
Elida. Onse amenewa ndi ana a Ketura. 5Ndipo Abrahamu amwali anampatsa
Isake zonse anali nazo. 6Koma kwa ana a akazi ace ang'ono amene Abrahamu
anali nao Abrahamu anapatsa mphatso, nawacotsa iwo kwa Isake mwana
wace, akali ndi moyo, kuti anke kum'mawa, ku dziko la kum'mawa. 7Masiku a
zaka za moyo wace wa Abrahamu amene anakhala ndi moyo ndiwo zaka zana
limodzi, kudza makumi asanu ndi limodzi, kudza khumi ndi zisanu. 8Ndipo
Abrahamu anamwalira, nafa m'ukalamba wace wabwino, nkhalamba ya zaka
zambiri; natengedwa akhale ndi a mtundu wace. 9Ndipo ana ace Isake ndi
Ismayeli anamuika iye m'phanga la Makipela, m'munda wa Efroni mwana wace
wa Zohari Mhiti, umene uli patsogolo pa Mamre; 10munda umene anagula
Abrahamu kwa ana a Heti: pamenepo anamuika Abrahamu ndi Sara mkazi
wace. 11Ndipo panali atafa Abrahamu, Mulungu anamdalitsa Isake mwana
wace; ndipo Isake anakhala pa Beere-lahai-roi.

Mbumba ya Ismayeli

12Mibadwo ya Ismayeli mwana wamwamuna wace wa Abrahamu, amene
Hagara M-aigupto mdzakazi wa Sara anambalira Abrahamu ndi iyi: 13ndipo
maina a ana a Ismayeli, maina ao m'mibadwo yao ndi awa: woyamba wa
Ismayeli ndi Nebayoti; ndi Kedara, ndi Abideele, ndi Mibisamu, 14ndi Misima,
ndi Duma; ndi Masa; 15ndi Hadada, ndi Tema, ndi Yeturi, ndi Nafisi, ndi
Kedema; 16ana a Ismayeli ndi awa: maina ao m'midzi yao, m'misasa yao ndi
awa: akaronga khumi ndi awiri m'mitundu yao. 17Zaka za moyo wa Ismayeli ndi
izi: zaka zana limodzi kudza makumi atatu ndi zisanu ndi ziwiri: ndipo iye
anamwalira, natengedwa akhale ndi a mtundu wace. 18Ndipo anakhala iwo
kuyambira ku Havila kufikira ku Suri, ndiko kum'mawa kwace kwa Aigupto,
pakunka ku Asuri: ndipo iye anakhala pamaso pa abale ace onse.

Esau ndi Yakobo

19Mibadwo ya Isake mwana wace wa Abrahamu ndi iyi: Abrahamu anabala
Isake: 20ndipo Isake anali wa zaka makumi anai pamene anakwata Rebeka,
mwana wamkazi wa Betuele Msuriya wa ku Padanaramu, mlongo wace wa
Labani Msuriya. 21Ndipo Isake anampembedzera mkazi wace kwa Yehova
popeza anali wouma: ndipo Yehova analola kupembedza kwace, ndipo Rebeka
mkazi wace anatenga pakati, 22Ndipo ana analimbana m'kati mwace: ndipo iye
anati, Ngati cotero, ine ndikhala ndi moyo bwanji? ndipo ananka kukafunsa kwa
Yehova. 23Yehova ndipo anati kwa iye,

Mitundu iwiri iri m'mimba mwako,
Magulu awiri a anthu adzaturuka m'mimba mwako;
Gulu lina lidzapambana mphamvu ndi linzace;
Wamkuru adzakhala kapolo wa wamng'ono.

24Atatha masiku ace akubala, taonani, amapasa anali m'mimba
mwace. 25Ndipo woyamba anabadwa wofiira, monse mwace monga maraya
aubweya; ndipo anamucha dzina lace Esau. 26Pambuyo pace ndipo anabadwa

mphwace ndipo dzanja lace linagwira citende ca Esau, ndi dzina lace linachedwa Yakobo: ndipo Isake anali wa zaka makumi asanu ndi limodzi pamene mkazi wace anabala iwo.

Esau agulitsa ukulu wace

27Ndipo anakula anyamatawo; ndipo Esau anali munthu wakudziwa zakusaka nyama, munthu wa m'thengo; ndipo Yakobo anali munthu wofatsa, wakukhala m'mahema. 28Ndipo Isake anakonda Esau, cifukwa anadya nyama yace ya m'thengo; koma Rebeka anakonda Yakobo, 29Ndipo Yakobo anaphika mphodza: ndipo Esau anacokera kuthengo, nalefuka: 30ndipo Esau anati kwa Yakobo, Undipatse ndidye cofiiraco; cifukwa ndalefuka: cifukwa cace anamucha dzina lace Edomu. 31Ndipo Yakobo anati, Tigulane lero ukulu wako. 32Ndipo Esau anati, Taona, ine ndifuna kufa: ukuluwo ndidzapindulanii nao? 33Ndipo anati Yakobo, Undilumbirire ine lero lomwe, ndipo analumbirira iye; nagulana ndi Yakobo ukulu wace. 34Ndipo Yakobo anampatsa Esau mkate ndi mphodza zophika; ndipo iye anadya, namwa, nanyamuka, napita; comweco Esau ananyoza ukulu wace.

Genesis 26

Isake akhala kwa Afilisti

1Ndipo panali njala padzikopo, yoyenjezeka ndi njala yoyamba ija imene inali masiku a Abrahamu, ndipo Isake ananka kwa Abimeleke mfumu ya Afilisti ku Gerari. 2Ndipo Yehova anamuonekera iye nati, Usatsikire ku Aigupto, khala m'dziko m'mene ndidzakuuza iwe; 3khala mlendo m'dziko muno, ndipo Ine ndidzakhala ndi iwe, ndipo ndidzadalitsa iwe cifukwa kuti ndidzakupatsa iwe ndi mbeu zako maiko onse awa, ndipo ndidzalimbikitsa cilumbiriro ndinacilumbirira kwa Abrahamu atate wako; 4ndipo ndidzacurukitsa mbeu zako monga nyenyezi za kumwamba, ndipo ndidzapatsa mbeu zako maiko onsewa; m'mbeu zako mitundu yonse ya dziko lapansi idzadalitsidwa; 5cifukwa kuti Abrahamu anamvera mau anga, nasunga cilangizo canga, ndi maweruziro anga, ndi malemba anga ndi malamulo anga. 6Ndipo Isake anakhala m'Gerari; 7ndipo anthu a kumeneko anamfunsa iye za mkazi wace; ndipo iye anati, diye mlongowanga: cifukwa kuti anaopa kunena, Mkazi wanga; anati, anthu a kumeneko angandiphe ine cifukwa ca Rebeka; popeza anali wokongola pakumuona. 8Ndipo panali atakhala komwe masiku ambiri, Abimeleke mfumu ya Afilisti, anayang'ana kunja kwa zenera, napenya, taona, Isake analinkuseka ndi Rebeka mkazi wace. 9Ndipo Abimeleke anamuitana Isake nati, Taona, uyo ndi mkazi wako ndithu: kodi bwanji unati, Ndiye mlongo wanga? Ndipo Isake anati kwa iye, Cifukwa ndinati, Ndingafe cifukwa ca iye. 10Ndipo Abimeleke anati, Nciani cimeneci waticitira ife? panatsala pang'ono ena a anthu akadagona naye mkazi wako, ndipo ukadaticimwitsa ife: 11Ndipo Abimeleke anauza anthu ace, nati, Ali yense amene akhudza mwamuna uyo kapena mkazi wace, zoonatu adzaphedwa. 12Ndipo Isake anabzala m'dzikomo, nalandira za makumi khumi caka cimeneco; ndipo Yehova anamdalitsa iye. 13Ndipo anakula munthuyo, nakulakula kufikira kuti anakhala wamkurukuru: 14ndipo anali ndi cuma ca nkhosa, ndi cuma ca zoweta, ndi banja lalikuru: ndipo Afilisti anamcitira iye nsanje. 15Ndipo zitsime zonse anakumba anyamata a atate wace Afilisti anazitseka, nazikwirira ndi dothi. 16Ndipo Abimeleke anati kwa Isake, Ucoke kwa ife cifukwa kuti iwe uti wamkuru wopambana ife. 17Ndipo Isake anacoka kumeneko, namanga hema wace m'cigwa ca Gerari, nakhala kumeneko. 18Ndipo Isake anafukulanso zitsime za madzi, anazikumba masiku a Abrahamu atate wace; cifukwa kuti Afilisti anazitseka atafa Abrahamu: ndipo anazicha maina monga maina omwe anazicha atate wace. 19Ndipo anyamata a Isake anakumba m'cigwa, napeza kumeneko citsime ca madzi otumphuka. 20Ndipo abusa a Gerari anakangana ndi abusa a Isake kuti, Madzi ndi athu; ndipo anacha dzina la citsimeco Eseke: cifukwa anakangana nave. 21Ndipo anakumbanso citsime cina, ndipo anakangana naconso; nacha dzina lace Sitina. 22Ndipo anacoka kumeneko nakumba citsime cina; koma sanakangana naco cimeneco; ndipo anacha dzina lace Rehoboti; ndipo anati, Cifukwa kuti tsopano Yehova anatipatsa ife malo, ndipo tidzabalana m'dziko muno. 23Ndipo anacoka kumeneko nakwera kunka ku Beereseba, 24Ndipo Yehova anamuonekera iye usiku womwewo, nati, Ine dine Mulungu wa Abrahamu atate wako; usaope, cifukwa kuti Ine ndiri ndi iwe, ndipo ndidzakudalitsa iwe, ndi kucurukitsa mbeu zako, cifukwa ca Abrahamu kapolo wanga. 25Ndipo anamanga kumeneko guwa la nsembe, naitana dzina la

Yehova, namanga hema wace kumeneko: ndi pamenepo anyamata a Isake anakumba citsime.

Isake apangana ndi Abimeleke

26Ndipo ananka kwa iye Abimeleke kucokera ku Gerari, ndi Ahuzati bwenzi lace, ndi Fikoli, kazembe wa nkhondo yace. 27Ndipo Isake anati kwa iwo, Mwandidzera cifukwa ciani, inu akundida ine, ndi kundicotsa kwanu? 28Ndipo iwo anati, Kuona tinaona kuti Yehova ali ndi iwe; ndipo tinati, Tilumbiriranetu tonse awiri, ife ndi iwe, ticite pangano ndi iwe; 29kuti usaticitire ife zoipa, pakuti sitidakhudza iwe, sitidakucirira kanthu koma kabwino ndiko, ndipo takulola umuke ndi mtendere; ndiwe tsopano wodalitsidwa ndi Yehova. 30Ndipo anakonzera iwo madyerero, ndipo anadya namwa. 31Ndipo analawira m'mamawa nalumbirirana wina ndi mnzace; ndipo Isake anawalola amuke, ndipo anauka kucokera kwa iye m'mtendere. 32Ndipo panali tsiku lomwelo anyamata ace a Isake anadza namuuza iye za citsime cimene anakumba, nati kwa iye, Tapeza madzi. 33Ndipo anacha dzina lace Seba, cifukwa cace dzina la mudziwo ndi Beereseba kufikira lero lino.

34Pamene Esau anali wa zaka makumi anai, anakwatira Yuditi mwana wamkazi wa Beeri Mhiti, ndi Basemati mwana wamkazi wa Elone Mhiti: 35ndipo iwo anapweteka mtima wa Isake ndi wa Rebeka.

Genesis 27

Yakobo adalitsidwa m'malo mwa Esau

1Ndipo panali atakalamba Isake, ndi maso ace anali a khungu losaona nalo, anamuitana Esau mwana wace wamwamuna wamkuru, nati kwa iye, Mwana wanga; ndipo anati kwa iye, Ndine pano. 2Ndipo anati, Taonatu, ndakalamba, sindidziwa tsiku la kufa kwanga: 3tsopano tengatu zida zako ndi phodo lako ndi uta wako, numuke kuthengo kundisakira ine nyama; 4nundikonzere ine cakudya cokolera conga comwe ndicikonda ine, nudze naco kwa ine kuti ndidzadye; kuti moyo wanga ukadalitse iwe ndisanafe. 5Ndipo anamva Rebeka pamene Isake ananena ndi Esau mwana wace. Ndipo Esau ananka kuthengo kukasaka nyama ndi kubwera nayo. 6Ndipo Rebeka ananena kwa Yakobo mwana wace, nati, Taona ndinamva atate wako alinkunena ndi Esau mkuru wako kuti, 7Unditengere ine nyama, undikonzere ine cakudya cokolera, kuti ndidzadye, ndi kudalitsa iwe pamaso pa Yehova, ndisanafe. 8Tsopanotu mwana wanga, tamvera mau anga monga momwe nditi ndikuuze iwe. 9Pitatu kubusa, ukanditengere ine kumeneko tiana tiwiri tabwino ta mbuzi; ndikonzere nato cakudya cokolera ca atate wako conga comwe acikonda: 10ndipo udzapita naco kwa atate wako, kuti adye, ndi kukudalitsa iwe asanafe, 11Yakobo ndipo anati kwa Rebeka amace, Taonani, Esau mkuru wanga ndiye munthu waubweya, ine ndine munthu, wosalala. 12Kapena atate wanga adzandiyambasa, ndipo ndidzaoneka pamaso pace ngati wakunyenga; pamenepo ndidzadzitengera ine temberero, si mdalitso. 13Ndipo amace anati kwa iye, Pa ine likhale temberero lako mwana wanga; koma tamvera mau anga, kazimuka kunditengera timeneto. 14Ndipo anamuka nakatenga nadza nato kwa amace; amace ndipo anakonza cakudya cokolera conga cimene anacikonda atate wace. 15Ndipo Rebeka anatenga zobvala zokoma za Esau, mwana wace wamkuru zinali m'nyumba, nabveka nazo Yakobo mwana wace wamng'ono; 16ndipo anabveka zikopa za tiana tambuzi pa manja ace ndi pakhosi pace posalala; 17ndipo anapereka m'dzanja la mwana wace Yakobo cakudya cokoleraco, ndi mikate imene anaipanga. 18Ndipo iye analowa kwa atate wace, nati, Atate wanga; iye anati, Ndine pano; ndani iwe mwana wanga? 19Ndipo Yakobo anati kwa atate wace, Ndine Esau mwana wanu wamkuru; ndacita monga mwandiuza ine; ukanitu, khalani tsonga, idyani nyama yanga kuti moyo wanu undidalitse ine. 20Ndipo Isake anati kwa mwana wace, Unaipeza msanga bwanji mwana wanga? Ndipo anati, Cifukwa kuti Yehova Mulungu wanu anandiyendetsa ine bwino. 21Ndipo Isake anati kwa Yakobo, Sendera kuno, ndikuyambase mwana wanga, ngati ndiwe mwana wanga Esau ndithu, kapena wina. 22Ndipo Yakobo anasendera kwa Isake atate wace, ndipo anamyambasa nati, Mau ndi mau a Yakobo, koma manja ndi manja a Esau. 23Ndipo sanazindikira iye, cifukwa kuti manja ace anali aubweya, onga manja a Esau mkuru wace; ndipo anamdalitsa iye. 24Ndipo anati, Kodi ndiwe mwana wanga weniweni Esau? ndipo anati, Ndine amene. 25Ndipo iye anati, Usendere nayo kwa ine, ndidye nyama ya mwana wanga, kuti moyo wanga ukudalitse iwe. Ndipo anasendera nayo kwa iye, nadya iye; ndipo anamtengera vinyo, namwa iye. 26Ndipo Isake atate wace anati kwa iye, Senderatu, undimpsompsone mwana wanga. 27Ndipo anasendera nampsompsona; ndipo anamva kununkhira kwa zobvala zace, namdalitsa, nati,

Taona, kununkhira kwa mwana wanga,
Kufanana ndi kununkhira kwa munda anaudalitsa Yehova;
28Mlungu akupatse iwe mame a kumwamba,
Ndi zonenepa za dziko lapansi,
Ndi tirigu wambiri ndi vinyo;
29Anthu akutumikire iwe,
Mitundu ikuweramire iwe;
Ucite ufumu pa abale ako,
Ana a amako akuweramire iwe;
Wotembererekа ali yense akutemberera iwe,
Wodalitsika ali yense akudalitsa iwe.
30Ndipo panali atatha Isake kumdalitsa Yakobo, ataturuka Yakobo pamaso pa Isake atate wace, Esau mkuru wace analowa kucokera kuthengo, 31Ndipo iyenso anakonza cakudya cokolera, nadza naco kwa atate wace, nati kwa atate wace, Auke atate wanga, adye nyama ya mwana wace, kuti moyo wanu undidalitse ine. 32Ndipo Isake atate wace anati kwa iye, Ndiwe yani? ndipo iye anati, Ndine mwana wanu woyamba Esau. 33Ndipo Isake ananthunthumira ndi kunthunthumira kwakukuru, nati, Ndani uja anatenga nyama, nadza nayo kwa ine, ndipo ndadyako zonse usadaloweiwe, ndipondamdalitsaiye? inde, adzadalitsika. 34Pamene Esau anamva mau a atate wace Isake, analira ndi kulira kwakukuru ndi kowawa kopambana, nati kwa atate wace, Mundidalitse ine, inenso atate wanga. 35Ndipo iye anati, Mphwako anadza monyenga, nalanda mdalitso wako. 36Ndipo iye anati, Kodi si ndico cifukwa anamucha dzina lace Yakobo? kuti wandinyenga ine kawiri aka; analanda ukulu wanga ndipo taonani, tsopano walanda mdalitso wanga. Ndipo anati, Kodi smunandisungira ine mdalitso? 37Ndipo anayankha Isake nati kwa Esau, paona, ndamuyesa iye mkuru wako, ndi abale ace onse ndampatsa iye akhale akapolo ace; ndakhazikitsa iye ndi tirigu ndi vinyo; nanga pamenepo mwana wanga, ndidzakucitira iwe ciani? 38Ndipo Esau anati kwa atate wace, Kodi muli nao mdalitso umodzi wokha, atate wanga? Mundidalitse ine, inenso, atate wanga, Ndipo Esau anakweza mau ace nalira. 39Ndipo Isake atate wace anayankha nati kwa iye,
Taona, pokhala pako mpa zonenepa za dziko lapansi,
Mpa mame a kumwamba akudzera komwe;
40Udzakhala ndi moyo ndi lupanga lako, nudzakhala kapolo wamphwako;
Ndipo padzakhalapamene udzapulumuka,
Udzacotsa gori lace pakhosi pako.
41Ndipo Esau anamuda Yakobo cifukwa ca mdalitso umene atate wace anamdalitsa nao: ndipo Esau anati m'mtima mwace, Masiku a maliro a atate wanga ayandikira; pamenepo ndipo ndidzamupha mphwanga Yakobo. 42Ndipo anauza Rebeka mau a Esau mwana wace wamkuru: ndipo iye anatumiza naitana Yakobo mwana wace wamng'ono, nati kwa iye, Taona, mkuru wako Esau, kunena za iwe, adzitonthoza yekha mtima wace kuti adzakupha iwe. 43Ndipo tsopane mwana wanga, tamvera mau anga: tauka, nuthawire kwa Labani mlongo wanga ku Harana; 44ukhale naye masiku akuwerengeka, mpaka wamcokera ukali wa mkuru wako; 45mpaka wakucokera mkwiyo wa mkuru

wako, kuti aiwale cimene wamcitira iye; pamenepo ndipo ndidzatumiza kukutenganso iwe kumeneko; ndidzakhala bwanji wopanda inu nonse awiri tsiku limodzi?

46 Ndipo anati Rebeka kwa Isake, Ndalema moyo wanga cifukwa ca aria akazi a Heti: akatenga Yakobo mkazi wa ana akazi a Heti, onga ana akazi a m'dziko lino, moyo wanga udzandikhalira ine bwanji?

Genesis 28

1Ndipo Isake anamuitana Yakobo, namdalitsa iye, namuuza iye, nati kwa iye, Usatenge mkazi wa ana akazi a Kanani. 2Tauka, nupite ku Padanaramu, ku nyumba ya Betuele, atate wa amai ako; ukadzitengere mkazi wa kumeneko kwa ana akazi a Labani mlongo wace wa amako. 3Mulungu Wamphamvuyonse akudalitse iwe, akubalitse iwe, akucurukitse iwe, kuti ukhale khamu la anthu: 4akupatse iwe mdalitso wa Abrahamu, iwe ndi mbeu zako pamodzi nawe: kuti ulowe m'dziko limene ukhalamo mlendo, limene Mulungu anampatsa Abrahamu. 5Ndipo Isake anamlola Yakobo amuke, ndipo ananka ku Padanaramu kwa Labani, mwana wace wa Betuele Msuriya, mlongo wace wa Rebeka, amai wao wa Yakobo ndi Esau.

Yakobo apita ku Padanaramu

6Ndipo anaona Esau kuti Isake anamdalitsa Yakobo namtumiza ku Padanaramu kuti atenge mkazi wa kumeneko; 7ndiponso kuti pamene anamdalitsa iye, anamuuza iye kuti, Usatenge mkazi wa ana akazi a Kanani; ndiponso kuti Yakobo anamvera atate wace ndi amace, nanka ku Padanaramu; 8ndipo Esau anaona kuti ana akazi a Kanani sanakondweretsa Isake atate wace: 9ndipo ananka kwa Ismayeli, naonjezera kwa akazi amene anali nao, natenga Mahalati mwana wamkazi wa Ismayeli mwana wa Abrahamu, mlongo wace wa Nebayoti akhalemkazi wace.

Loto la Yakobo ku Beteli

10Ndipo Yakobo anacoka m'Beereseba, nanka ku Harana. 11Ndipo anafika kumalo, nagona kumeneko usiku, cifukwa lidalowa dzuwa: ndipo anatenga mwala wa kumeneko, nauika pansi pa mutu wace, nagona tulo kumeneko. 12Ndipo analota, taonani, makwerero anaima pansi, pamwamba pace ndipo padafikira kumwamba: ndipo, taonani, amithenga a Mulungu analinkukwera, analinkutsika pamenepo. 13Taonani, Yehova anaima pamwamba pace, nati, Ine ndine Yehova, Mulungu wa Abrahamu atate wako, ndi Mulungu wa Isake; dziko limene ulinkugonamo ndidzakupatsa Iwe ndi mbeu zako; 14mbeu zako zidzakhala monga pfumbi lapansi, ndipo udzabalalikira kumadzulo ndi kum'mawa ndi kumpoto ndi kumwera: mwa iwe ndi mu mbeu zako mabanja onse a dziko lapansi adzadalitsidwa. 15Taonani, Ine ndiri pamodzi ndi iwe, ndipo ndidzakusunga iwe konse kumene upitako, ndipo ndidzakubwezanso iwe ku dziko lino; cifukwa kuti sindidzakusiya iwe, kufikira kuti nditacita cimene ndanena nawe. 16Ndipo Yakobo anauka m'tulo tace, nati, Ndithu, Yehova ali mommuno; ndipo sindinadziwe. 17Ndipo anaopa, nati, Poopsya pompano! pompano ndipo pa nyumba ya Mulunga, si penai, pompano ndipo pa cipata ca kumwamba. 18Yakobo ndipo anauka m'mamawa, natenga mwala umene anaika pansi pa mutu wace, nauimiritsa, nathira mafuta pamtu pace. 19Ndipo anacha dzina la pamenepo Beteli; pakuyamba dzina lace la mudziwo ndi Luzi. 20Yakobo ndipo analumbiracilumbiro, nati, Mulungu akakhala ndi ine, akandisunga ine m'njira imene ndipitamo, akandipatsa ine mkate wa kudya, ndi zobvalira za kubvala, 21kuti ndibwerenso ku nyumba ya atate wanga ndi mtendere, pamenepo Yehova adzakhala Mulungu wanga, 22ndi mwala umenewu ndinauimiritsa, udzakhala nyumba ya Mulungu; ndipo la zonse mudzandipatsa ine, ndidzakupatsani Inu limodzi la magawo khumi.

Genesis 29

Yakobo akomana ndi Rakele

1Ndipo Yakobo ananka ulendo wace, nafika ku dziko la anthu a
kum'mawa. 2Ndipo anayang'ana, taonani, citsime m'dambo, ndipo, taonani,
magulu atatu a nkhosa alinkugona kumeneko: pakuti pacitsimepo anamwetsa
nkhosa; ndipo mwala wa pakamwa pa citsime unali waukuru. 3Kumeneko ndipo
zinasonkhana zoweta zonse: ndipo anagubuduza mwala kuucotsa pakamwa pa
citsime, namwetsa nkhosa, naikanso mwala pakamwa pa citsime pamalo
pace. 4Ndipo anati Yakobo kwa iwo, Abale anga, ndinu a kuti inu? nati, Ndife a
ku Harana. 5Ndipo anati kwa iwo, Kodi mumdziwa Labani mwana wace wa
Nahori? nati, Timdziwa. 6Ndipo anati kwa iwo, Kodi ali bwino? nati, Ali bwino:
taonani, Rakele mwana wace wamkazi alinkudza nazo nkhosa. 7Ndipo iye
anati, Taonani, kukali msana, si nthawi yosonkhanitsa zoweta; mwetsani
nkhosa, pitani, kadyetseni. 8Ndipo anati, Sitingathe, koma zitasonkhana ziweto
zonse, ndipo atagubuduza mwala kuucotsa pakamwa pa citsime ndiko;
pamenepo ndipo tizimwetsa nkhosa. 9Ali cilankhulire nao, anafika Rakele ndi
nkhosa za atate wace, cifukwa anaziweta. 10Ndipo panali pamene Yakobo
anaona Rakele, mwana wamkazi wa Labani, mlongo wace wa amace, ndi
nkhosa za Labani mlongo wace wa amace, Yakobo anayandikira nagubuduza
kuucotsa mwala pacitsime, nazimwetsa zoweta za Labani, mlongo wace wa
amace. 11Ndipo Yakobo anampsompsona Rakele nakweza mau ace,
nalira. 12Ndipo Yakobo anamuuza Rakele kuti iye ndiye mbalewace wa atate
wace, kuti ndiye mwana wace wa Rebeka, ndipo Rakele anathamanga nakauza
atate wace.

Labani alandira Yakobo

13Ndipo panali pamene Labani anamva mbiri ya Yakobo mwana wa mlongo
wace, iye anathamangira kukakomana naye namfungatira, nampsompsona,
namlowetsa m'nyumba mwace. Ndipo iye anamfotokozera Labani zinthu
zonsezo. 14Ndipo Labani anati kwa iye, Etu, iwe ndiwe pfupa langa ndi thupi
langa. Ndipo anakhala naye nthawi ya mwezi umodzi. 15Ndipo Labani anati
kwa Yakobo, Cifukwa iwe ndiwe mbale wanga, kodi udzanditumikira ine
kwacabe? Undiuze ine, malipiro ako adzakhala otani? 16Ndipo Labani anali ndi
ana akazi awiri, dzina la wamkuru ndi Leya, dzina la wamng'ono ndi
Rakele. 17Maso a Leya anali ofok a, koma Rakele anali wokoma thupi ndi
wokongola. 18Ndipo Yakobo anamkonda Rakele, nati, Ndidzakutumikirani inu
zaka zisanu ndi ziwiri cifukwa ca Rakele mwana wanu wamkazi
wamng'ono. 19Ndipo anati Labani, Kuli kwabwino kuti ndimpatse iwe
osampatsa kwa mwamuna wina; ukhalebe ndi ine. 20Ndipo Yakobo
anamtumikira zaka zisanu ndi ziwiri cifukwa ca Rakele; koma zidamuonekera
iye ngati masiku owerengeka cifukwa ca cikondi cimene anamkonda iye naco.

Leya ndi Rakele

21Ndipo Yakobo anati kwa Labani, Undipatse Ine mkazi wanga, cifukwa masiku
anga atha, kuti ndilowe kwa iye. 22Ndipo Labani anasonkhanitsa anthu onse a
kumeneko nakonzera madyerero. 23Ndipo panali madzulo Labani anatenga
Leya mwana wace wamkazi, nadza naye kwa Yakobo, ndipo iye analowa kwa
mkaziyo. 24Ndipo Labani anampatsa mwana wace wamkazi Leya Zilipa
mdzakazi wace kuti akhale mdzakazi wa Leya. 25Ndipo panali m'mamawa,

anaona kuti ndi Leya; ndipo anati kwa Labani, Ciani wandicitira ine? Kodi sindinakutumikira iwe cifukwa ca Rakele? wandinyenga ine bwanji? 26Ndipo Labani anati, Satero kwathu kuno, kupatsa wamng'ono asanapatse wamkuru. 27Umarize sabata lace la uyu, ndipo ndidzakupatsa uyonso cifukwa ca utumiki umene udzanditumikirawo kuonjezera zaka zina zisanu ndi ziwiri. 28Yakobo ndipo anacita cotero namariza sabata lace; ndipo Labani anampatsa iye Rakele mwana wace wamkazi kuti akwatire iyenso. 29Ndipo Labani anampatsa mwana wace wamkazi Rakele Biliha mdzakazi wace kuti akhale mdzakazi wa Rakele. 30Ndipo Yakobo analowanso kwa Rakele, namkondanso Rakele kopambana Leya, namtumikira Labani zaka zisanu ndi ziwiri zinanso.

Ana a Yakobo

31Pamene Yehova anaona kuti anamuda Leva, anatsegula m'mimba mwace; koma Rakele anali wouma. 32Ndipo Leyaanatenga pakati, nabala mwana wamwamuna, namucha dzina lace Rubeni; pakuti anati, Cifukwa kuti tsopano mwamuna wanga adzandikonda ine. 33Ndipo anatenganso pakati, nabala mwana wamwamuna nati, Cifukwa anamva Yehova kuti anandida ine, anandipatsa ine mwana wamwamuna uyunso; ndipo anamucha dzina lace Simeoni. 34Ndipo anatenganso pakati nabala mwana wamwamuna, nati, Tsopano lino mwamuna wanga adzadziphatika kwa ine cifukwa ndambalira iye ana amuna atatu; cifukwa cace anamucha dzina lace Levi. 35Ndipo anatenganso pakati nabala mwana wamwamuna; nati, Tsopano ndidzamyamikira Yehova; cifukwa cace anamucha dzina lace Yuda; pamenepo analeka kubala.

Genesis 30

1Pamene Rakele anaona kuti sanambalira Yakobo ana, Rakele anamcitira
mkuru wace nsanje; nati kwa Yakobo, Ndipatse ana ndingafe. 2Ndipo Yakobo
anapsa mtima ndi Rakele; nati, Kodi ine ndikhala m'malo a Mulungu amene
akukaniza iwe zipatso za mimba? 3Ndipo Rakele anati, Taonani mdzakazi
wanga Biliha, mulowe kwa iye; ndipo iye adzabala pa maondo anga, kuti inenso
ndionerepo ana pa iye. 4Ndipo Rakele anampatsa iye Biliha mdzakazi wace
akhale mkazi wace; ndipo Yakobo analowa kwa iye. 5Ndipo Biliha anatenga
pakati, nambalira Yakobo mwana wamwamuna. 6Rakele ndipo anati, Mulungu
wandiweruzira ine, namva mau anga, nandipatsa ine mwana; cifukwa cace
anamucha dzina lace Dani. 7Ndipo Biliha mdzakazi wace wa Rakele
anatenganso pakati, nambalira Yakobo mwana wamwamuna waciwiri. 8Ndipo
Rakele anati, Ndi malimbano a Mulungu ndalimbana naye mkuru wanga, ndipo
ndapambana naye; ndipo anamucha dzina lace Nafitali. 9Pamene Leya anaona
kuti analeka kubala, anatenga Zilipa mdzakazi wace, nampatsa iye kwa Yakobo
kuti akhale mkazi wace. 10Ndipo Zilipa mdzakazi wace wa Leya anambalira
Yakobo mwana wamwamuna. 11Ndipo Leyaanati, Wamwai ine! ndipo
anamucha dzina lace Gadi. 12Ndipo Zilipa mdzakazi wa Leya anambalira
Yakobo mwana wamwamuna waciwiri. 13Ndipo Leya anati, Ndakondwa inel
cifukwa kuti ana akazi adzandicha ine wokondwa: ndipo anamucha dzina lace
Aseri. 14Ndipo Rubeni ananka masiku akudula tirigu, napeza zipatso za
mankhwala a cikondi m'thengo, nazitengera kwa amace Leva, Ndipo Rakele
anati kwa Leya, Undipatseko mankhwala a mwana wako. 15Ndipo iye anati kwa
Rakele, Kodi mpacabe kuti iwe wacotsa mwamuna wanga? Kodi ufuna
kucotsanso mankhwala a mwana wanga? Rakele ndipo anati, Cifukwa cace iye
adaagona nawe usiku uno cifukwa ca mankhwala a mwana wako. 16Ndipo
Yakobo anadza madzulo kucokera kumunda, ndipo Leya ananka kukomana
naye, nati, Ulowe kwa ine cifukwa ndakulipilira iwe ndi mankhwala a mwana
wanga. Ndipo anagona naye usiku womwewo. 17Ndipo Mulungu anamvera
Leya, ndipo anatenga pakati, nambalira Yakobo mwana wamwamuna
wacisanu. 18Ndipo Leya anati, Mulungu wandipatsa ine mphotho yanga,
cifukwa ndapatsa mdzakazi wanga kwa mwamuna wanga: namucha dzina lace
lsakara. 19Ndipo Leya anatenganso pakati nambalira Yakobo mwana
wamwamuna wacisanu ndi cimodzi. 20Ndipo Leya anati, Mulungu anandipatsa
ine mphatso yabwino; tsopane mwamuna wanga adzakhala ndi ine, cifukwa
ndambalira iye ana amuna asanu ndi mmodzi; ndipo anamucha dzina lace
Zebuloni. 21Pambuyo pace ndipo anabala mwana wamkazi, namucha dzina
lace Dina. 22Ndipo Mulungu anakumbukila Rakele, ndipo Mulungu anamvera
iye, natsegula m'mimba mwace. 23Ndipo anatenga pakati, nabala mwana
wamwamuna, nati, Mulungu wacotsa manyazi anga; 24namucha dzina lace
Yosefe; ndipo anati, Yehova anandionjezera ine mwana wamwamuna wina.

Laban; apangana ndi Yakobo

25Ndipo panali pamene Rakele anabala Yosefe, Yakobo anati kwa Labani,
Undisudzule ine ndinke kwathu ku dziko langa. 26Undipatse ine akazi anga ndi
ana anga cifukwa ca iwowa ndakutumikira iwe, ndimuke: cifukwa udziwa iwe
nchito imene ndinakugwirira iwe. 27Ndipo Labani anati kwa iye, Ngatitu
ndikapeza ufulu pamaso pako, ukhale, cifukwa ndazindikira kuti Yehova

wandidalitsa ine cifukwa ca iwe. 28Ndipo iye anati, Undipangire ine malipiro ako, ndipo ndidzakupatsa. 29Ndipo iye anati kwa Labani, Udziwa iwe comwe ndakutumikira iwe ndi comwe zacita zoweta zako ndi ine. 30Cifukwa ndisadafike ine, iwe unali nazo zowerengeka, ndipo zacuruka zambirimbiri; Yehova wakudalitsa iwe kuli konse ndinayendako: tsopano ndidzamanga liti banja langa? 31Ndipo iye anati, Ndikupatsa iwe bwanji? Ndipo Yakobo anati, Usandipatse ine kanthu; ukandicitira ine cotero, ine ndidzadyetsanso ndi kusunganso ziweto zako. 32Ndidzapita ine lero pakati pa ziweto zonse ndi kusankhasankha m'menemo zoweta zonse zamathotho-mathotho ndi zamaanga-maanga, ndi za nkhosa zonse, ndi mbuzi zonse zamaangamaanga ndi zamathotho-mathotho: zotero zidzakhala malipiro anga. 33Cotero cilungamo canga cidzandibvomereza m'tsogolomo, pamene udzandifika cifukwa ca malipiro amene ali patsogolo pako; iri yonse yosakhala yamathotho-mathotho ndi yamaanga-maanga ya mbuzi, ndi iri yonse ya mbuzi yosakhala yakuda, ikapezedwa ndi ine, udzaiyesa yakuba. 34Ndipo Labani anati, Taona, kukhale monga mau ako. 35Tsiku lomwelo Labani anacotsa atonde amene anali amipyololo-mipyololo ndi amathotho-mathotho, ndi mbuzi zazikazi zinali zamaanga-maanga ndi zamathotho-mathotho zonse zinali zoyera pang'ono, ndi zakuda zonse za nkhosa, napatsa m'dzanja la ana ace amuna. 36Ndipo iye yekha anatalikitsana ndi Yakobo ulendo wa masiku atatu: ndipo Yakobo anadyetsa ziweto zina za Labani. 37Ndipo Yakobo anatenga nthyole za mtengo wowisi walibne, ndi za mtengo wakatungurume, ndi za mtengo waarimoni, nakupula m'menemo mizere yoyera, naonetsa moyera mwa m'nthyolemo. 38Ndipo anaimitsa nthyole zimene anazikupula pandunji ndi zoweta m'micera yakumwera, m'mene ziweto zinafika kumweramo, ndipo zidatenga mabere pamene zinadza kumwa. 39Ndipo ziweto zinatenga mabere patsogolo pa nthyolezo, ndipo zoweta zinabala zamipyololomipyololo, ndi mathotho-mathotho, ndi zamaanga-maanga. 40Ndipo Yakobo analekanitsa ana a nkhosa naziika nkhope za zoweta kuti ziyang'anire zamipyololo-mipyololo, ndi zakuda zonse za m'zoweta za Labani, ndipo anaika magulu ace pa okha; sanaziika pa zoweta za Labani. 41Ndipo panali pamene zoweta zolimba zidatenga mabere, Yakobo anaika nthyole pamaso pa zoweta m'miceramo kuti zitenge mabere pa nthyolezo. 42Koma pamene ziweto zinali zofoka, sanaziika zimenezo: ndipo zofoka zinali za Labani, ndi zolimba zinali za Yakobo. 43Munthuyo ndipo anakula kwambiri, nali nazo zoweta zambiri, ndi akapolo amuna ndi akazi, ndi ngamila, ndi aburu.

Genesis 31

1Yakobo afuna kwao nathawa nazo zace, Ndipo anamva mau a ana ace a Labani kuti, Yakobo watenga zonse za atate wathu; m'zinthu zinali za atate wathu wapeza iye cuma ici conse. 2Ndipo Yakobo anaona nkhope ya Labani, taonani, siinamuonekera iye monga kale. 3Ndipo Yehova anati kwa Yakobo, Bwera ku dziko la atate wako, ndi kwa abale ako, ndipo ndidzakhala ndi iwe. 4Ndipo Yakobo anatumiza naitana Rakele ndi Leya adze kubusa ku zoweta zace, 5ndipo anati kwa iwo, Ndiona ine nkhope ya atate wanu kuti siindionekera ine monga kale; koma Mulungu wa atate wanga anali ndi ine. 6Ndipo inu mudziwa kuti ndi mphamvu zanga zonse ndatumikira atate wanu. 7Ndipo atate wanu wandinyenga ine, nasinthanitsa malipilo anga kakhumi; koma Mulungu sanamlole iye andicitire ine coipa. 8Akati cotero, Zamathotho-mathotho zidzakhala malipilo ako, zoweta zonse zinabala zamathotho-mathotho; ndipo akati iye cotere, Zamipyololo-mipyololo zidzakhala malipilo ako, ziweto zonse zinabala mipyololo-mipyololo. 9Comweco Mulungu anazicotsa zoweta za atate wanu, nandipatsa ine. 10Ndipo panali potenga mabere ziwetozo, ine ndinatukula maso anga, ndipo ndinapenya m'kulota, taonani, atonde okwera ziweto anali amipyololo-mipyololo, amathotho-mathotho, ndi amaanga-maanga. 11Mthenga wa Mulungu ndipo anati kwa ine m'kulotamo, Yakobo; nati ine, Ndine pano, 12Ndipo anati, Tukulatu maso ako, nuone, atonde onse amene akwera zoweta ali amipyololo-mipyololo, amathotho-mathotho, ndi amaangamaanga: cifukwa ndaona zonse zimene Labani akucitira iwe. 13Ine ndine Mulungu wa ku Beteli, kuja unathira mafuta pamwala paja, pamene unandilumbirira ine cilumbiriro: tsopano uka, nucoke m'dziko lino, nubwerere ku dziko la abale ako. 14Ndipo Rakele ndi Leya anayankha, nati kwa iye, Kodi tiri nalonso gawo kapena colowa m'nyumba ya atate wathu? 15Kodi satiyesa ife alendo? cifukwa anatigulitsa ife, nathanso kuononga ndalama zathu. 16Cifukwa kuti cuma conse Mulungu anacicotsa kwa atate wathu ndi cathu ndi ca ana athu; tsono, zonse wakunenera iwe Mulungu, ucite. 17Ndipo anauka Yakobo nakweza ana ace ndi akazi ace pa ngamila; 18ndipo ananka nazo zoweta zace zonse, ndi cuma cace conse anacisonkhanitsa, zoweta zace anaziona m'Padan-aramu, kuti anke kwa Isake atate wace ku dziko la Kanani. 19Ndipo Labani ananka kukasenga nkhosa zace: ndipo Rakele anaba aterafi a atate wace. 20Ndipo Yakobo anathawa kwa Labani Msuriyamobisika, m'mene sanamuuzeiye kuti analinkuthawa. 21Ndipo anathawa iye ndi zonse anali nazo: ndipo anauka naoloka panyanja naloza nkhope yace iyaog'anire ku phiri la Gileadi.

Labani alondola wothawayo

22Tsiku lacitatu anamuuza Labani kuti Yakobo wathawa. 23Ndipo iye anatenga abale ace pamodzi naye, namlondola iye ulendo wa masiku asanu ndi awiri: nampeza iye pa phiri la Gileadi. 24Ndipo Mulungu anadza kwa Labani Msuriya usiku, nati kwa iye, Tadziyang'anira wekha, usanene kwa Yakobo kapena zabwino kapena zoipa, 25Ndipo Labani anakomana naye Yakobo. Ndipo Yakobo anamanga hema wace m'phirimo: ndipo Labani ndi abale ace anamanga m'phiri la Gileadi. 26Ndipo Labani anati kwa Yakobo, Wacitanji? Wathawa kwa ine mobisika ndi kutenga ana anga akazi, monga mikoli ya lupanga. 27Wathawanji iwe mobisika, ndi kundicokera kutseri, osandiuza ine, kuti ndikadakumukitsa iwe ndi kusekerera ndi nyimbo ndi lingaka ndi

zeze? 28Ndipo sunandiloleza ine ndimpsompsone ana anga amuna ndi akazi? wapusa iwe pakucita cotero. 29M'dzanja langa muli mphamvu yakucitira iwe zoipa koma Mulungu wa atate wako anati kwa ine usiku walero, kuti, Tadziyang'anira wekha, usanene kwa Yakobo kapena zabwino kapena zoipa. 30Tsono ungakhale ukadamuka cifukwa mtima wako ulinkukhumba nyumba ya atate wako, bwanji waba iwe milungu yanga? 31Ndipo anayankha Yakobo nati kwa Labani, Cifukwa ndinaopa: cifukwa kuti, ndinati, Kapena udzandilanda ine ana ako akazi. 32Ali yense umpeza ali nayo milungu yako, asakhale ndi movo: pamaso pa abale athu, tayang'anira zako ziri ndi ine, nuzitenge wekha. Pakuti sanadziwe Yakobo kuti Rakele anaiba. 33Ndipo Labani analowa m'hema wa Yakobo, ndi m'hema wa Leya, ndi m'mahema a adzakazi awiri aja; koma sanapeze, Ndipo anaturuka m'hema wa Leya nalowa m'hema wa Rakele. 34Ndipo Rakele anatenga aterafiwo nabisa pa cokhalira ca ngamila, nakhala pamenepo, Ndipo Labani anafunafuna m'hema monse, koma sanawapeze. 35Ndipo Rakele anati kwa atate wace, Asakwiye mbuyanga kuti sindingathe kuuka pamaso panu; cifukwa zocitika pa akazi ziri pa ine. Ndipo Labani anafunafuna koma sanapeze aterafiwo. 36Ndipo anakwiya Yakobo namkalipira Labani: ndipo Yakobo anayankha nati kwa Labani, Kodi ndacimwa ciani? ucimo wanga nguti, kuti unanditsatatsata ine pambuyo panga? 37Pakuti wafunafuna monse ndiri nazo, kodi wapeza ciani pa zinthu za m'nyumba mwako? Tafika naco apa pa abale anga ndi ako, kuti aweruze pa ife tonse awiri. 38Zaka makumi awiriwo ndakhala nawe, nkhosa ndi mbuzi zako zazikazi sizinapoloze, ndi abira a zoweta zako sindinadye. 39Cimene cinazomoledwa ndi cirombo sindinacitengere kwa iwe; ndekha ndinalipira; pa dzanja langa unacifuna, cingakhale cobedwa kapena pausiku kapena pausana. 40Cotero ndinakhala; usana ludzu linakomola ine, usiku cisanu; tulo tanga tinacoka m'maso mwanga. 41Ndinakhala cotere zaka makumi awiri m'nyumba mwako; zaka khumi ndi zinai ndinakutumikira iwe cifukwa ca ana ako akazi awiri, ndi zaka zisanu ndi cimodzi cifukwa ca zoweta zako; wasintha malipiro anga kakhumi. 42Mulungu wa atate wanga, Mulungu wa Abrahamu, ndi Kuopsa kwa Isake zikadapanda kukhala ndi ine, ukadandicotsa ine wopanda kanthu m'manja. Mulungu anakuona kusauka kwanga, ndi nchito ya manja anga, ndipo anadzudzula iwe usiku walero.

Labani apangana ndi Yakobo

43Ndipo Labani anayankha nati kwa Yakobo, Akaziwa ndiwo ana anga, anawa ndiwo ana anga, zowetazi ndizo zoweta zanga ndi zonse ulinkuziona ndizo zanga: nanga ndidzacitira ine ciani lero kwa ana anga akazi amenewa, kapena ana ao amene anabala? 44Tsopano tiyeni tipangane pangano, ine ndi iwe; likhale mboni pakati pa ine ndi iwe. 45Ndipo Yakobo anatenga mwala, nauimiritsa. 46Ndipo Yakobo anati kwa abale ace, Sonkhanitsani miyala; ndipo anasonkhanitsa miyala nakundika mulu: ndipo anadya pamulupo. 47Ndipo Labani anacha pamenepo Yegara-sahaduta; koma Yakobo anacha Galeeda. 48Ndipo Labani anati, Muluwu ndiwo mboni pakati pa ine ndi iwe lero. Cifukwa cace anacha dzina lace, Galeeda; 49ndi Mizipa, cifukwa kuti anati, Yehova ayang'anire pakati pa ine ndi iwe, pamene tisiyana wina ndi mnzace. 50Ukasautsa ana anga akazi, kapena ukatenga akazi kuonjezera pa

ana anga, palibe munthu mmodzi ali nafe; taonani, Mulungu ndiye mboni yanga ndi yako. 51Ndipo Labani anati kwa Yakobo. Taona muluwu, taona coimiritsaci, ndaciimiritsa pakati pathu. 52Muluwu ndiwo mboni, coimiritsaci ndico mboni, kuti ine sindidzapitirira pa muluwu kunka kwa iwe, ndipo iwe sudzapitirira pa muluwu ndi pa coimiritsaci kudza kwa ine kuti ticitirane zoipa, 53Mulungu wa Abrahamu ndi Mulungu wa Nahori, Mulungu wa atate wao aweruze pa ife. Ndipo Yakobo analumbirira pa Kuopsa kwa atate wace Isake. 54Ndipo Yakobo anapereka nsembe paphiripo, naitana abale ace kuti adye cakudya; ndipo anadya cakudya, nagona paphiripo usiku wonse. 55M'mamawa Labani anauka nampsompsona ana ace amuna ndi akazi, nawadalitsa: ndipo Labani anacoka, nabwera kumalo kwace.

1Ndipo Yakobo anankabe ulendo wace, ndipo amithenga a Mulungu
anakomana naye. 2Pamene Yakobo anawaona anati, Ili ndi khamu la Mulungu:
ndipo anacha pamenepo dzina lace Mahanaimu.

Yakobo akonzekeratu kukomana ndi Esau

3Ndipo Yakobo anatumiza amithenga patsogolo pace kwa Esau mkuru wace,
ku dziko la Seiri, ku dera la ku Edomu. 4Ndipo anauza iwo kuti, Mukanene
cotere kwa mbuyanga Esau: Atero Yakobo kapolo wako, ndakhala pamodzi
naye Labani, ndipo ndakhalabe kufikira tsopano line: 5ndipo ndiri nazo ng'ombe
ndi aburu, ndi zoweta ndi akapolo ndi adzakazi, ndipo ndatumiza kukuuza
mbuyanga kuti ndipeze ufulu pamaso pako. 6Ndipo amithenga anabwera kwa
Yakobo kuti, Tidafika kwa mbale wanu Esau, ndipo iyenso alinkudza kukomana
nanu, ndipo ali nao anthu mazana anai. 7Ndipo Yakobo anaopa kwambiri,
nabvutidwa; ndipo anagawa anthu anali nao ndi nkhosa ndi zoweta, ndi
ngamila, zikhale makamu awiri; 8ndipo anati, Akafika Esau pa khamu limodzi
nalikantha, linalo lotsala lidzapulumuka. 9Ndipo Yakobo anati, Mulungu wa
atate wanga Abrahamu, Mulungu wa atate wanga Isake, Yehova, amene munati
kwa ine, Bwera ku dziko lako, ndi kwa abale ako, ndipo ndidzakucitira iwe
bwino: 10sindiyenera zazing'ono za zifundo zonse, ndi zoona zonse, zimene
mwamcitira kapolo wanu: cifukwa ndi ndodo yanga ndinaoloka pa Yordano uyu;
ndipo tsopano ndiri makamu awiri. 11Mundipulumutsetu ine m'dzanja la mkuru
wanga, m'dzanja la Esau; cifukwa ine ndimuopa iye, kapena adzadza
kudzandikantha ine, ndi amai pamodzi ndi ana. 12Ndipo Inu munati.
Ndidzakucitira iwe bwino ndithu, ndidzakuyesa mbeu yako monga mcenga wa
pa nyanja yaikuru, umene sungathe kuwerengeka cifukwa ca unyinji
wace. 13Ndipo anagona komweko usiku womwewo, natengako zimene anali
nazo, mphatso yakupatsa Esau mkuru wace: 14mbuzi zazikazi mazana awiri,
atonde makumi awiri, nkhosa zazikazi mazana awiri, ndi zazimuna makumi
awiri, 15ngamila zamkaka makumi atatu ndi ana ao, ng'ombe zazikazi makumi
anai, zazimuna khumi, aburu akazi makumi awiri ndi ana khumi. 16Ndipo
anazipereka zimenezo m'manja a anyamata ace, gulu pa lokha gulu pa lokha:
ndipo anati kwa anyamata ace, Taolokani patsogolo panga, tacitani danga
pakati pa magulu, tina ndi lina. 17Ndipo anauza wotsogolera kuti, Pamene
akomana nawe mkuru wanga Esau ndi kufunsa iwe kuti, Ndiwe yani, umuka
kuti? za yani zimenezi patsogolo pako? 18pomwepo uziti, Za kapolo wanu
Yakobo; ndizo mphatso yotumizidwa kwa mbuyanga Esau; taonani ali pambuyo
pathu. 19Ndipo anauzanso waciwiri ndi wacitatu, ndi onse anatsata magulu,
kuti, Muzinena kwa Esau cotero, pamene mukomana naye: 20ndiponso muziti,
Ndiponso, taonani, kapolo wanu Yakobo ali pambuyo pathu, Pakuti anati,
Ndidzampembedzera iye ndi mphatso imene ipita patsogolo panga, pambuyo
pace ndidzaona nkhope yace; kapena adzandilandira ine. 21Momwemo
naolotsa mphatso patsogolo pace: ndipo iye yekha anagona usiku womwewo
pacigono.

Yakobo alimbana ndi mngelo nalandira dzina latsopano

22Ndipo anauka usiku womwewo, natenga akazi ace awiri, ndi adzakazi ace
awiri, ndi ana ace amuna khumi ndi mmodzi, naoloka pa doko la
Yaboki. 23Ndipo anawatenga iwo nawaolotsa pamtsinje, naziolotsa

zonseanalinazo. 24Ndipo anatsala Yakobo yekha; ndipo analimbana naye munthu kufikira mbandakuca. 25Ndipo pamene anaona kuti sanamlaka, anakhudza nsukunyu ya ncafu yace; ndipo nsukunyu ya ncafu yace ya Yakobo inaguluka, pakulimbana naye. 26Ndipo iye anati Ndileke ndimuke, cifukwa kulinkuca. Ndipo Yakobo anati, Sindidzakuleka iwe kuti umuke, ukapanda kundidalitsa ine. 27Ndipo iye anati kwa Yakobo, Dzina lako ndani? Nati iye, Yakobo. 28Ndipo anati, Dzina lako silidzachedwanso Yakobo, koma Israyeli, cifukwa unayesana naye Mulungu ndithu, ndipo unapambana. 29Yakobo ndipo anafunsa iye, nati, Undiuze ine dzina lako. Ndipo iye anati, Undifunsa dzina cifukwa ninji? Ndipo anamdalitsa iye pamenepo. 30Ndipo anacha dzina la malo amenewo, Penieli: cifukwa ndaonana ndi Mulungu nkhope ndi nkhope, ndipo wapulumuka moyo wanga, 31Ndipo kudamcera iye pamene analoloka pa Penieli, ndipo iye anatsimphina ndi ncafu yace. 32Cifukwa cace ana a Israyeli samadya ntsempha ya thako iri pa nsukunyu ya ncafu kufikira lero: cifukwa anakhudza nsukunyu ya ncafu ya Yakobo pa ntsempha ya thako.

Genesis 33

Yakobo ayanjanidwa ndi Esau

1Ndipo Yakobo anatukula maso ace, taonani, anadza Esau, ndi pamodzi naye
anthu mazana anai. Ndipo anagawira ana kwa Leya, ndi kwa Rakele, ndi kwa
adzakazi awiri aja. 2Ndipo anaika adzakazi ndi ana ao patsogolo, ndi Leya ndi
ana ace pambuyo pao, ndi Rakele ndi Yosefe pambuyo pa onse. 3Ndipo iye
mwini anatsogolera patsogolo pao, nawerama pansi kasanu ndi kawiri mpaka
anayandikira mkuru wace. 4Ndipo Esau anathamangira kukomana naye
namfungatira, nagwa pankhope pace, nampsompsona; ndipo analira
iwo. 5Ndipo anatukula maso ace nawaona akazi ndi ana; nati, Ndani awa ali ndi
iwe? Ndipo iye anati, Ndiwo ana amene Mulungu anakomera mtima kumpatsa
kapolo wanu. 6Ndipo adzakazi anayandikira ndi ana ao, nawerama
pansi. 7Ndiponso Leya ndi ana ace anayandikira nawerama pansi: pambuyo
pace anayandikira Yosefe ndi Rakele, nawerama pansi, 8Ndipo anati, Nanga
khamu lonse limene ndinakomana nalo nlotani? Ndipo anati, Kuti ndipeze ufulu
pamaso pa mbuyanga. 9Ndipo Esau anati, Zanga zindifikira; mbale wanga,
khala nazo zako iwe wekha. 10Ndipo! Yakobo anati, Iaitu, ngatitu ndapeza ufulu
pamaso panu, mulandire mphatso yanga pa dzanja langa; pakuti popeza
ndinaona nkhope yanu, monga anthu aona nkhope ya Mulungu, ndipo inu
mwanelibvomereza ine. 11Landiranitu mdalitso wanga umene wafika kwa inu,
pakuti Mulungu wandicitira ine zaufulu, ndipo zanganso zindifikira. Ndipo
anamkakamiza, nalandira. 12Ndipo Esau anati, Tiyeni timuke; nditsogolera
ndine. 13Ndipo anati kwa iye, Mbuyanga adziwa kuti ana ali ambowa, ndipo
nkhosa ndi zoweta ndiri nazo zirinkuyamwitsa: ndipo akathamangitsa tsiku
limodzi zoweta zonse zidzafa. 14Mbuyanga atsogoleretu kapolo wace, ndipo
ine ndidzazitsogolera pango'no-pang'ono monga mwa mayendedwe a zoweta
ziri pamaso panga, ndi monga mwa mayendedwe a ana, mpaka ndifike kwa
mbuyanga ku Seiri. 15Ndipo Esau anati, Ndikusiyire anthu ena amene ali ndi
ine, Ndipo iye anati, Cifukwa canji? ndipeze ine ufulu pamaso pa
mbuyanga. 16Ndipo Esau anabwera tsiku lomwelo kunka ku Seiri. 17Ndipo
Yakobo anankabe ulendo wace ku Sukoti, namanga nyumba yace pamenepo,
namanga makola a zoweta zace: cifukwa cace dzina lace la kumeneko ndi
Sukoti.

Yakobo afika ku Sekemu

18Ndipo Yakobo anafika ndi mtendere ku mudzi wa Sekemu umene uli m'dziko
la Kanani, pamene anacokera ku Padanaramu; namanga tsasa pandunji pa
mudzipo. 19Ndipo anagula ndi ndalama zana limodzi dera la munda kumeneko
anamanga bema wace, pa dzanja la ana ace a Hamori atate wace wa
Sekemu. 20Ndipo anamanga pamenepo guwa la nsembe, nacha pamenepo
ElelohaIsrayeli.

Genesis 34

Dina ndi a Sekemu

1Ndipo Dina mwana wamkazi wa Leya, amene anambalira Yakobo, ananka
kukaona akazi a kumeneko. 2Pamene anamuona iye Sekemu, mwana wace
wamwamuna wa Hamori Mhivi, karonga wa dzikolo, anamtenga nagona ndi iye,
namuipitsa, 3Ndipo mtima wace unakhumba Dina mwana wace wamkazi wa
Yakobo, ndipo anamkonda namwaliyo, nanena momkopa namwaliyo. 4Ndipo
anati Sekemu kwa atate wace Hamori kuti, Munditengere ine mkazi uyo akhale
mkazi wanga. 5Ndipo anamva Yakobo kuti anamuipitsa Dina, mwana wace
wamkazi; ana ace amuna anali ndi zoweta zace kudambo: ndipo Yakobo
anakhala cete mpaka anafika iwo. 6Ndipo Hamori atate wace wa Sekemu
anaturuka kunka kwa Yakobo kukanena ndi iye. 7Ndipo pakumva ico ana ace
amuna a Yakobo anabwera pocokera kudambo: amunawo ndipo
anaphwetekwa mtima, nakwiya kwambiri, cifukwa iyeyo anacita copusa coipira
Israyeli pakugona ndi mwana wamkazi wa Yakobo; ndico cosayenera
kucita. 8Ndipo Hamori ananena ndi iwo, kuti, Mtima wa Sekemu mwana wanga
umkhumba mwana wako wamkazi: umpatsetu kuti akhale mkazi
wace. 9Mukwatirane ndi ife: tipatseni ife ana anu akazi, ndiponso dzitengereni
ana athu akazi. 10Ndipo mudzakhala pamodzi ndi ife, dziko lidzakhala pamaso
panu; khalani m'menemo ndi kucita malonda, ndi kukhala nazo zanuzanu
m'menemo. 11Ndipo Sekemu anati kwa atate wace wa mkazi ndi kwa abale
ace, Tipeze ufulu pamaso panu, cimene mudzanena kwa ine
ndidzapereka. 12Mundipemphe ine za mitulo ndi zaulere zambirimbiri, ndipo
ndidzapereka monga mudzanena kwa ine; koma mundipatse ine namwaliyo
akhale mkazi wanga. 13Ndipo ana ace amuna a Yakobo anayankha Sekemu
ndi Hamori atate wace monyenga, nanena, popeza anamuipitsa Dina mlongo
wao, 14nati kwa iwo, Sitingathe kucita ici, kupereka mlongo wathu kwa
mwamuna wosadulidwa; cifukwa kumeneko ndiko kuticepetsa ife. 15Koma apa
pokha tidzakubvomerezani: ngati mudzakhala onga ife ndi kudulidwa amuna
onse; 16pamenepo tidzakupatsani inu ana athu akazi, ndipo tidzadzitengera
ana anu akazi, ndipo tidzakhala pamodzi ndi inu, ndi kukhala mtundu
umodzi. 17Koma mukapanda kutimvera ndi kusadulidwa, pamenepo tidzatenga
mwana wathu wamkazi, ndi kumuka naye. 18Mau ao ndipo anakomera Hamori
ndi Sekemu mwana wace wa Hamori. 19Ndipo mnyamatayo sanacedwa
kucicita popeza anakondwera ndi mwana wace wamkazi wa Yakobo; ndipo iye
anali wolemekezedwa woposa onse a pa banja la atate wace. 20Ndipo Hamori
ndi Sekemu mwana wace anafika ku cipata ca mudzi wao, nalankhulana ndi
anthu a mudzi wao, kuti, 21Anthu amenewa ali amtendere pamodzi ndi ife;
cifukwa cace akhale m'dzikomo, acite malonda m'menemo: pakuti taonani
dzikololirilalikurulokwaniraiwo; tidzitengere ana ao akazi akhale akazi athu,
tiwapatse amenewa ana athu akazi. 22Anthuwo adzatiloleza ife tikhale nao
anthu amodzi, pokhapo amuna onse a mwa ife adzadulidwa, monga iwo
adulidwa. 23Kodi ng'ombe zao ndi cuma cao ndi zoweta zao sizidzakhala
zathu? Pokhapo tibvomerezana nao ndipo adzakhala pamodzi ndi ife. 24Ndipo
onse amene anaturuka pa cipata ca mudzi wao anamvera Hamori ndi mwana
wace Sekemu, nadulidwa amuna onse akuturuka pa cipata ca mudzi
wao. 25Ndipo panali tsiku lacitatu pamene anamva kuwawa, ana amuna awiri a

Yakobo, Simeoni ndi Levi, abale ace a Dina, anatenga wina lupanga lace wina lace, nalimbika mtima nalowa m'mudzi napha amuna onse. 26Ndipo anapha Hamori ndi Sekemu mwana wace ndi lupanga, naturutsa Dina m'nyumba ya Sekemu nacoka naye. 27Ndipo ana amuna a Yakobo anadzakwa ophedwa nafunkhamudzi cifukwa anamuipitsa mlongo wao. 28Ndipo analanda nkhosa zao ndi zoweta zao ndi aburu ao, ndi za m'mudzi, ndi za m'munda; 29ndi cuma cao conse ndi ana ao ndi akazi ao anawagwira, nafunkha zonse za m'nyumba. 30Ndipo Yakobo anati kwa Simeoni ndi Levi, Mwaodisautsa ndi kundinunkhitsa ine mwa anthu okhala m'dzikomu, mwa Akanani ndi mwa Aperezi; ndipo ine ndine wa anthu owerengeka, adzandisonkhanira ine ndi kundikantha: ndipo ndidzapasulidwa ine ndi a pa nyumba yanga. 31Ndipo iwo anati, Kodi iye ayenera kusandutsamloogo wathu wadama?

Genesis 35

Yakobo amanga ku Beteli

1Ndipo Mulungu anati kwa Yakobo, Nyamuka nukwere kunka ku Beteli nukhale kumeneko: numange kumeneko guwa la nsembe la Mulungu amene anaonekera kwa iwe pamene unathawa ku nkhope ya Esau mbale wako. 2Ndipo Yakobo anati kwa a banja lace, ndi kwa onse amene anali ndi iye, Cotsani milungu yacilendo iri mwa inu, mudziyeretse, ndi kupindula zobvala zanu: 3tinyamuke, tikwere tinke ku Beteli: ndipo tidzamanga kumeneko guwa la nsembe la Mulungu amene anandibvomereza tsiku la mabvuto anga, ndiponso anali ndi ine m'njira m'mene ndinapitamo. 4Ndipo anampatsa Yakobo milungu yacilendo yonse inali m'manja mwao, ndi mphete zinali m'makutu mwao: ndipo Yakobo anazibisa pansi pa mtengo wathundu unali pa Sekemu. 5Ndipo anapita, ndipo kuopsa kwa Mulungu kudagwera midzi yakuwazinga, ndipo sanalondola ana a Yakobo. 6Ndipo Yakobo anafika ku Luzi, ndiko ku dziko la Kanani (ndiwo Beteli), iye ndi anthu onse anali pamodzi ndi iye. 7Ndipo anamanga kumeneko guwa la nsembe, Dacha pamenepo El Beteli: pakuti kumeneko Mulungu anaonekera kwa iye muja anathawa pa nkhope ya mbale wace. 8Ndipo anafa Debora mlezi wa Rebeka, naikidwa kunsi kwa Beteli, pansi pa mtengo wathundu; ndipo anacha dzina lace AlioniBakuti.

9Ndipo Mulungu anamuonekeranso Yakobo, pamene iye anacokera m'Padanaramu, namdalitsa iye. 10Ndipo Mulungu anati kwa iye, Dzina lako ndi Yakobo; dzina lako silidzachedwanso Yakobo, koma dzina lako lidzakhala Israyeli: ndipo anamucha dzina lace Israyeli. 11Ndipo Mulungu anati kwa iye, Ine ndine Mulungu Wamphamvuyonse: ubale, ucuruke; mwa iwe mudzaturuka mtundu ndi gulu la mitundu, ndipo mafumu adzaturuka m'cuuno mwako; 12ndipo dziko limene ndinapatsa kwa Abrahamu ndi kwa Isake ndidzalipatsa kwa iwe ndipo ndidzapatsa mbeu zako za pambuyo pako dzikoli. 13Ndipo Mulungu anakwera kumcokera iye kumene ananena naye. 14Ndipo Yakoboanaimiritsamwala pamalo pamene ananena ndi iye, coimiritsa camwala: ndipo anathira pamenepo nsembe yothira, nathirapo mafuta. 15Ndipo anacha dzina lace la pamalo pamene Mulungu ananena ndi iye, Beteli.

Rakele amwalira pobadwa Benjamini

16Ndipo anacokera ku Beteli: ndipo panatsala nthawi asanafike ku Efrati: ndipo Rakele anabala nabvutidwa. 17Ndipo panali pamene anabvutidwa, namwino anati kwa iye, Usaope: pakuti udzakhala ndi mwana wina wamwamuna. 18Ndipo pakutsirizika iye, pakuti anamwalira, anamucha dzina lace Benoni; koma atate wace anamucha Benjamini. 19Ndipo anafa Rakele, naikidwa pa njira va ku Efrati (ndipo Betelehemu), 20Ndipo Yakobo anaimiritsa mwala pamanda pace: umenewo ndi coimiritsa ca pa manda a Rakele kufikira lero. 21Ndipo Israyeli anapita namanga hema wace patseri pa nsanja ya Edere. 22Ndipo panali pamene Israyeli anakhala m'dzikomo, Rubeni anamuka nagona ndi Biliha, mkazi wamng'ono wa atate wace: ndipo Israyeli anamva.

Ana amuna a Yakobo anali khumi ndi awiri: 23ana amuna a Leya: ndiwo Rubeni mwana woyamba wa Yakobo, ndi Simeoni ndi Levi, ndi Yuda, ndi Zebuloni, ndi Isakara; 24ana amuna a Rakele: ndiwo Yosefe ndi Benjamini; 25ana amuna a Biliha mdzakazi wace wa Rakele: ndiwo Dani ndi Nafitali; 26ndipo ana amuna a

Zilipa mdzakazi wace wa Leya: ndiwo Gadi ndi Aseri: amenewo ndi ana amuna a Yakobo amene anabala iye m'Padanaramu. 27Ndipo Yakobo anafika kwa Isake atate wace ku Mamre, ku KiriyatiAriba (ndiwo Hebroni) kumene anakhala Abrahamu ndi Isake. 28Ndipo masiku a Isake anali zaka zana limodzi kudza makumi asanu ndi atatu. 29Ndipo Isake anatsirizika nafa, nasonkhanitsidwa kwa anthu a mtundu wace, wokalamba ndi wa masiku okwanira: ndipo Esau ndi Yakobo ana ace amuna anamuika iye.

Genesis 36

Mbumba ya Esau

1Mibadwo ya Esau (ndiye Edomu) ndi iyi: 2Esau anatenga akazi ace a ana
akazi a m'Kanani: Ada mwana wamkazi wa Eloni Mhiti, ndi Oholibama mwana
wamkazi wa Ana, mwana wamkazi wa Zibeoni Mhivi; 3ndi Basemati mwana
wamkazi wa lsmayeli, mlongo wace wa Nabayoti. 4Ndipo Ada anambalira Esau
Elifazi; ndipo Basemati anabala Reueli; 5ndipo Oholibama anabala Jeusi, ndi
Jalamu, ndi Kora; amenewa ndi ana amuna a Esau, amene anambadwira
m'dziko la Kanani. 6Ndipo Esau anatenga akazi ace, ndi ana ace amuna, ndi
ana ace akazi, ndi anthu onse a m'banja mwace, ndi ng'ombe zace, ndi zoweta
zace, ndi zonse anali nazo anasonkhanitsa m'dziko la Kanani; ndipo ananka ku
dziko losiyana patari ndi Yakobo mphwace. 7Cifukwa cuma cao cinali cambiri
cotero kuti sanakhoza kukhala pamodzi; ndipo dziko lokhalamo iwo silinakhoza
kuwakwanira cifukwa ca ng'ombe zao. 8Ndipo Esau anakhala m'phiri la Seiri;
Esau ndiye Edomu. 9Mibadwo ya Esau atate wao wa Aedomu m'phiri la Seiri
ndi iyi: 10amenewa ndi maina a ana amuna a Esau: Elifazi mwana
wamwamuna wa Ada, mkazi wace wa Esau, Reueli mwana wamwamuna wa
Basemati mkazi wace wa Esau. 11Ndipo ana amuna a Elifazi ndiwo Temani,
Omari, Zefo ndi Gatamu, ndi Kenazi. 12Ndipo Timna anali mkazi wace
wamng'ono wa Elifazi mwana wamwamuna wa Esau; ndipo anambalira Elifazi
Amaleki: amenewa ndi ana amuna a Ada mkazi wace wa Esau. 13Ndi ana
amuna a Reueli: Nahati, ndi Zera, Sama, ndi Miza; amenewa ndi ana a
Basemati mkazi wace wa Esau. 14Ana amuna a Oholibama mwana wamkazi
wa Ana, mwana wamkazi wa Zibeoni, mkazi wace wa Esau, ndi awa: ndipo iye
anambalira Esau Jeusi, ndi Jalamu, ndi Kora. 15Amenewa ndi mafumu a ana
amuna a Esau: ana amuna a Elifazi woyamba wa Esau: mfumu Temani, mfumu
Omari, mfumu Zefo, mfumu Kenazi, 16mfumu Kora, mfumu Gatamu, mfumu
Amaleki: amenewa ndi mafumu a kwa Elifazi m'dziko la Edomu: amenewa ndi
ana amuna a Ada. 17Amenewa ndi ana amuna a Reueli mwana wamwamuna
wa Esau: mfumu Nahati, mfumu Zera, mfumu Sama, mfumu Miza; amenewa
ndi mafumu obadwa kwa Reueli m'dziko la Edomu: amenewa ndi ana amuna a
Basemati mkazi wace wa Esau. 18Amenewa ndi ana amuna a Oholibama
mkazi wace wa Esau; mfumu Jeusi, mfumu Jalamu, mfumu Kora, amenewa ndi
mafumu obadwa kwa Oholibama mwana wamkazi wa Ana, mkazi wace wa
Esau. 19Amenewa ndi ana amuna a Esau, amenewa ndi mafumu ao; yemweyo
ndi Edomu.

20Amenewa ndi ana amuna a Seiri Mhori, okhala m'dzikomo: Lotani ndi
Sobala, ndi Zibeoni, ndi Ana, 21ndi Disoni ndi Ezeri ndi Disani; amenewa ndi
mafumu obadwa kwa Ahori, ana a Seiri, m'dziko la Edomu. 22Ndi ana a Lotani
anali Hori ndi Hemamu: mlongo wace wa Lotani anali Timna. 23Ana a Sobali
ndi awa: Alivani ndi Manahati ndi Ebali, Sefo ndi Onamu. 24Ana a Zibeoni ndi
amenewa: Aia ndi Ana; ameneyo ndiye Ana uja anapeza akasupe a madzi
amoto m'cipululu, pakudyetsa aburu a Zibeoni atate wace. 25Ana a Ana ndi
awa: Disoni ndi Oholibama mwana wamkazi wa Ana. 26Ana a Disoni ndi awa:
Hemadani ndi Esibani ndi Itirani, ndi Kerana. 27Ana a Ezeri ndi awa: Biliha, ndi
Zavani, ndi Akani. 28Ana a Disoni ndi awa: Uzi ndi Arana. 29Mafumu obadwa
kwa Ahori: mfumu Lotani, mfumu Sobali, mfumu Zibeoni, mfumu Ana, 30mfumu

Disoni, mfumu Ezeri, mfumu Disani; amenewa ndi mafumu obadwa kwa Ahori, monga mwa maufumu ao m'dziko la Seiri.
31Amenewo ndi mafumu analamulira m'dziko la Edomu, asadalamulire ana a Israyeli mfumu ali yense. 32Ndipo Bela mwana wamwamuna wa Beori, analamulira m'Edomu, ndipo dzina la mudzi wace ndilo Dinaba. 33Ndipo Bela anamwalira, ndipo Jobabi mwana wamwamuna wa Zera wa ku Bozara analamulira m'malomwace. 34Ndipo Jobabi anamwalira, ndipo Husami wa ku dziko la Atemani analamulira m'malo mwaceo 35Ndipo Husami anamwalira, ndipo Hadadi mwana wamwamuna wa Bedadi, amene anakantha Midyani m'dambo la Moabu, analamulira m'malo mwace: dzina la mudzi wace ndi Avita. 36Ndipo Hadadi anamwalira, ndipo Samila wa ku Masereka analamulira m'malo mwace. 37Ndipo Samila anamwalira, ndipo Sauli wa ku Rehoboti pambali pa Nyanja analamulira m'malo mwaceo 38Ndipo Sauli anamwalira, ndipo Baal-hanani mwana wamwamuna wa Akibori analamulira m'malo mwace. 39Ndipo Baal-hanani mwana wamwamuna wa Akibori anamwalira, ndipo Hadari analamulira m'malo mwace; dzina la mudzi wace ndi Pau; ndipo dzina la mkazi wace ndi Mehetabeli, mwana wamkazi wa Matiredi, mwana wamkazi wa Me-zahabi. 40Maina a mafumu obadwa kwa Esau, monga mabanja ao, monga malo ao, monga maina ao ndi awa: mfumu Timna, mfumu Aliva, mfumu Jeteti: 41mfumu Oholibama, mfumu Ela, mfumu Pinoni; 42mfumu Kenazi, mfumu Temani, mfumu Mibezari; 43mfumu Magidieli, mfumu Iramu; amenewa ndi mafumu a Edomu, monga mwa kukhala kwao m'dziko lokhala laolao. Uyo ndiye Esau atate wao wa Aedomu.

Genesis 37

Yosefe agulitsidwa ndi abale ace

1Ndipo Yakobo anakhala m'dziko limene anakhalamo mlendo atate wace,
m'dziko la Kanani. 2Mibadwo ya Yakobo ndi iyi: Yosefe anali wa zaka khumi ndi
zisanu ndi ziwiri analinkudyetsa zoweta pamodzi ndi abale ace; ndipo anali
mnyamata pamodzi ndi ana a Biliha, ndi ana amuna a Zilipa, akazi a atate
wace; ndipo Yosefe anamfotokozera atate wace mbiri yao yoipa. 3Koma Israyeli
anamkonda Yosefe koposa ana ace onse, pakuti anali mwana wa ukalamba
wace; ndipo anamsokera iye malaya amwinjiro. 4Ndipo abale ace anaona kuti
atate wace anamkonda iye koposa abale ace onse: ndipo anamuda iye, ndipo
sanathe kulankhula ndi iye mwamtendere. 5Yosefe ndipo analota loto,
nawafotokozera abale ace; ndipo anamuda iye koposa. 6Ndipo iye anati kwa
iwo, Tamvanitu loto limene ndalota: 7pakuti taonani, ndinalinkumanga mitolo
m'munda, ndipo taonani, mtolo wanga unauka nuima ciriri! ndipo taonani, mitolo
yanu inadza niuzinga kwete, niuweramira mtolo wanga. 8Abale ace ndipo anati
kwa iye, Kodi udzakhala mfumu yathu ndithu? kapena udzatilamulira ife ndithu
kodi? ndipo anamuda Iye koposa cifukwa ca maloto ace ndi mau ace. 9Ndipo
analotanso lata lina, nafotokozera abale ace, nati, Taonani, ndalotanso lata lina:
ndipo taonani, dzuwa ndi mwezi ndi nyenyezi khumi ndi imodzi zinandiweramira
ine. 10Ndipo iye anafotokozera atate wace ndi abale ace; ndipo atate wace
anamdzudzula, nati kwa iye, Loto limene walota iwe nlotani? Kodi ine ndi amai
ako ndi abale ako tidzafika ndithu tokha kuweramira iwe pansi? 11Ndipo abale
ace anamcitira iye nsanje, koma atate wace anasunga mau amene m'mtima
mwace. 12Ndipo abale ace ananka kukaweta zoweta za atate wao
m'Sekemu. 13Ndipo Israyeli anati kwa Yosefe, Kodi abale ako sadyetsa zoweta
m'Sekemu? tiyeni, ndikutuma iwe kwa iwo. Ndipo anati, Ndine pano. 14Ndipo
anati kwa iye, Pita tsopano, nukaone ngati abale ako ali bwino, ndi ngati zoweta
ziri bwino; nundibwezere ine mau. Ndipo anamtuma iye kucokera m'cigwa ca
Hebroni, ndipo anadza ku Sekemu. 15Ndipo anampeza munthu, taonani,
analinkusokera m'thengo; munthuyo ndipo anamfunsa, nati, Kodi ufuna
ciani? 16Ndipo iye anati, Ndifuna abale anga. Undiuzetu kumene adyetsa
zoweta. 17Munthuyo ndipo anati, Anacoka pano; pakuti ndinamva alinkuti,
Timuke ku Dotana. Yosefe ndipo anatsata abale ace, nawapeza ali ku
Dotana. 18Ndipo iwo anamuona iye ali patari, ndipo asanayandikire pafupi ndi
iwo, anampangira iye ciwembu kuti amuphe. 19Ndipo anati wina ndi mnzace,
Taonani, alinkudza mwini maloto uja. 20Tiyeni tsopano timuphe iye timponye
m'dzenje, ndipo tidzati, Wajiwa ndi cirombo; ndipo tidzaona momwe adzacita
maloto ace. 21Ndipo Rubeni anamva nampulumutsa iye m'manja mwao; nati,
Tisamuphe iye, 22Ndipo Rubeni anati kwa iwo, Musakhetse mwazi; mponyeni
iye m'dzenjemo m'cipululu muno, koma musamsamulire iye manja: kuti
ampulumutse iye ra'manja mwao, ambwezenso kwa atate wace. 23Ndipo
panali pamene Yosefe anafika kwa abale ace, anambvula Yosefe malaya ace,
malaya amwinjiro amene anabvala iye; 24ndipo anamtenga iye, namponya
m'dzenjemo; m'dzenjemo munalibe kanthu, munalibe madzi
m'menemo. 25Ndipo iwo anakhala pansi kuti adye cakudya; ndipo anatukula
maso ao, nayang'ana, ndipo taonani, ulendo wa Aismayeli anacokera ku Gileadi
ndi ngamila zao, zilinkunyamula zonunkhira ndi mafuta amankhwala ndi libano

alinkumuka kutsikira nazo ku Aigupto. 26Ndipo Yuda anati kwa abale ace, Nanga tidzapindulanji tikamupha mbale wathu ndi kufotsera mwazi wace? 27Tiyeni timgulitse iye kwa Aismayeli, tisasamulire iye manja; cifukwa ndiye mbale wathu, thupi lathu. Ndipo anamvera iye abale ace. 28Ndipo ana pita pamenepo Amidyani a malonda: ndipo anamturutsa namkweza Yosefem'dzenjemo, namgulitsa kwa Aismayeli ndi ndalama zasiliva makumi awiri; ndipo ananka naye Yosefe ku Aigupto.
29Ndipo Rubeni anabwera kudzenje, ndipo taonani, Yosefe mulibe m'dzenjemo: ndipo iye anang'amba nsaru yace. 30Ndipo anabwera kwa abale ace, nati, Mwana palibe; ndipo ine ndipita kuti? 31Ndipo anatenga malaya ace a Yosefe, napha tonde, nabvika malaya m'mwazi wace: 32natumiza malaya amwinjiro, nadza nao kwa atate ao: ndipo anati, Siwa tawatola; muzindikire tsono ngati ndi malaya a mwana wanu, kapena ndi ena. 33Ndipo anazindikira nati, Ndiwo malaya a mwana wanga: wajiwa ndi cirombo: Yosefe wakadzulidwa ndithu. 34Yakobo ndipo anang'amba malaya ace, nabvala ciguduli m'cuuno mwace namlirira mwana wace masiku ambiri. 35Ndipo ana amuna ace onse ndi ana akazi onse anauka kuti amtonthoze: koma anakana kutonthozedwa; ndipo anati, Pakuti ndidzatsikira kumanda kwa mwana wanga, ndirinkulirabe. Atate wace ndipo anamlirira. 36Amidyani ndipo anamgulitsa iye anke ku Aigupto kwa Potifara, nduna ya Farao, kazembe wa alonda.

Genesis 38

Yuda ndi Tamara

1Ndipo panali nthawi yomweyo, kuti Yuda anatsikira kwa abale ace nalowa kwa M-adulami, dzina lace Hira. 2Ndipo Yuda anaona kumeneko mwana wamkazi wa Mkanani dzina lace Sua: ndipo anamtenga, nalowa kwa iye. 3Ndipo anatenga pakati, nabala mwana wamwamuna, namucha dzina lace Eri. 4Ndipo anatenganso pakati, nabala mwana wamwamuna, namucha dzina lace Onani. 5Ndipo anabalanso mwana wamwamuna, namucha dzina lace Sela: ndipo iye anali pa Kezibi pamene mkazi anambala iye, 6Ndipo Yuda anamtengera Eri mwana wace woyamba mkazi, ndipo dzina lace ndilo Tamara. 7Koma Eri mwana wace woyamba wa Yuda anali woipa pamaso pa Yehova: ndipo Yehova anamupha iye. 8Ndipo Yuda anati kwa Onani, Lowani naye mkazi wa mbale wako, ndi kumcitira mkazi zoyenera mphwace wa mwamuna wace, ndi kumuukitsira mkuru wako mbeu. 9Ndipo Onani anadziwa kuti mbeu siidzakhala yace: ndipo panali pamene iye analowana naye mkazi wa mbale wace, kuti anaitaya pansi, kuti angampatse mbeu kwa mkuru wace. 10Koma cimene iye anacita cinali coipa pamaso pa Mulungu, ndipo anamupha iyenso. 11Ndipo Yuda anati kwa Tamara mpengozi wace, Khala wamasiye m'nyumba ya atate wako, kufikira akakula msinkhu Sela mwana wanga wamwamuna; cifukwa anati kuti, Angafe iyenso monga abale ace. Ndipo Tamara ananka nakhala m'nyumba ya atate wace. 12Atacuruka masiku mwana wamkazi wa Sua, mkazi wace wa Yuda anafa; ndipo Yuda anatonthola mtima, nakwera kunka kwa akusenga nkhosa zace ku Timna, iye ndi bwenzi lace Hira, M-adulami. 13Ndipo anamuuza Tamara, kuti, Taona, mpongozi wako akwera kunka ku Timna kuti akasenge nkhosa zace. 14Pamenepo anabvula zobvala zacezamasiye, nadzipfundandi copfunda cace, nabvala nakhala pa cipata ca Enaimu, cifukwa ciri pa njira ya ku Timna; pakuti anaona kuti Sela anakula msinkhu, ndipo sanampatsa iye kuti akhale mkazi wace. 15Pamene Yuda anamuona iye, anaganizira kuti ali mkazi wadama: cifukwa iye anabisa nkhope yace. 16Ndipo iye anapatukira kwa mkazi panjira, nati, Tiyetu, ndilowane nawe; cifukwa sanamdziwa kuti ndiye mpongozi wace. Ndipo anati, Kodi udzandipatsa ine ciani kuti ulowane ndi ine. 17Ndipo iye anati, Ndidzatumiza kwa iwe kamwana ka mbuzi ka m'ziweto. Ndipo mkazi nati, Kodi udzandipatsa ine cikole mpaka ukatumiza? 18Ndipo iye anati, Cikole canji ndidzakupatsa iwe? Ndipo mkazi anati, Mphete yako, ndi cingwe cako, ndi ndodo iri m'dzanja lako. Ndipo anampatsa izo, nalowana naye, ndipo mkazi anatenga pakati ndi iye. 19Ndipo mkazi anauka nacoka, nabvula copfunda cace, nabvala zobvala zamasiye zace. 20Ndipo Yuda anatumiza kamwana ka mbuzi ndi dzanja la bwenzi lace Madulami, kuti alandire cikole pa dzanja la mkazi; koma sanampeza iye. 21Ndipo anafunsa amuna a pamenepo kuti, Ali kuti wadama uja anali pambali pa njira pa Enaimu? ndipo iwo anati, Panalibe wadama pano. 22Ndipo iye anabwera kwa Yuda nati, Sitinampeza mkazi; ndiponso amuna a pamenepo anati, Panalibe wadama pano. 23Ndipo Yuda anati, Azilandire kuti tingacitidwe manyazi: taona, ndinatumiza mwana uyu wa mbuzi, ndipo sunampeza iye. 24Ndipo panali itapita miyezi itatu, anamuuza Yuda kuti, Tamara mpongozi wako wacita cigololo, ndiponso taonani, ali ndi pakati ndi cigololoco. Ndipo Yuda anati, Mturutse iye kuti amponye pamoto. 25Pamene anamturutsa Iye,

mkazi anatumiza kwa mpongozi wace kuti, Ndi mwamuna mwini izi ndatenga pakati; ndipo mkazi anati, Tayang'anatu, za yani zimenezi, mphete, ndi cingwe, ndi ndodo? 26Ndipo Yuda anabvomereza nati, Akhale wolungama wopambana ine, cifukwa ine sindinampatsa iye Sela mwana wanga wamwamuna. Ndipo iye sanamdziwanso mkaziyo. 27Ndipo panali nthawi ya kubala kwace, taonani, amapasa anali m'mimba mwace. 28Ndipo panali pamene anabala kuti mmodzi anaturutsa dzanja; ndipo namwino anatenga cingwe cofiira namanga pa dzanja lace, kuti, Uyu anayamba kubadwa. 29Ndipo panali pamene iye ana bweza dzanja lace, kuti, taona, mbale wace anabadwa, ndipo namwino anati, Wadziposolera wekha bwanji? cifukwa cace dzina lace linachedwa Pereze. 30Ndipo pambuyo pace anabadwa mbale wace, amene anali ndi cingwe cofiira pamkono pace, dzina lace linachedwa Zera.

Genesis 39

Yosefe ayesedwa ndi mkazi wa Potifara

1Ndipo anatsika naye Yosefe kunka ku Aigupto; ndipo Potifara, nduna ya Farao,
kazembe wa alonda, Maigupto, anamgula iye m'manja mwa Aismayeli amene
anatsika naye kunka iumeneko. 2Ndipo Yehova anali ndi Yosefe; ndipo iye anali
wolemeralemera; nakhala m'nyumba ya mbuyace M-aigupto. 3Ndipo mbuyace
anaona kuti Yehova anali ndi iye, ndi kuti Yehova anamlemereza m'dzanja lace
zonse anazicita. 4Ndipo Yosefe anapeza ufulu pamaso pace, ndipo
anamtumikira iye; ndipo anamuyesa iye woyang'anira pa nyumba yace, naika
m'manja mwace zonse anali nazo. 5Ndipo panali ciyambire anamuyesa iye
woyang'anira pa nyumba yace, ndi pa zace zonse, Yehova anadalitsa nyumba
ya M-aigupto cifukwa ca Yosefe; ndipo mdalitso wa Yehova unali pa zace
zonse, m'nyumba ndi m'munda. 6Ndipo iye anasiya zace zonse m'manja a
Yosefe; osadziwa comwe anali naco, koma cakudya cimene anadya. Ndipo
Yosefe anali wokoma thupi ndi wokongola. 7Ndipo panali zitapita izi, kuti mkazi
wa mbuyace anamyang'anira maso Yosefe: ndipo mkaziyo anati, Gona ndi
ine. 8Koma iye anakana, nati kwa mkazi wa mbuyace, Taonani, mbuyanga
sadziwa cimene ciri ndi ine m'nyumbamu, ndipo anaika zace zonse m'manja
anga; 9mulibe wina m'nyumba wamkuru ndine; ndipo sanandikaniza ine kanthu,
koma iwe, cifukwa kuti uli mkazi wace: nanga ndikacita coipa cacikuru ici bwanji
ndi kucimwira Mulungu? 10Ndipo pali pakunenanena ndi Yosefe tsiku ndi tsiku,
iye sanamvera mkazi kugona naye kapena kukhala naye. 11Ndipo panali,
nthawi yomweyo, iye analowa m'nyumba kuti agwire nchito yace; ndipo
munalibe amuna a m'nyumba m'katimo. 12Ndipo mkazi anagwira iye copfunda
cace, nati, Gona ndi ine; ndipo anasiya copfunda cace m'dzanja lace nathawa,
naturukira kubwalo. 13Ndipo panali pamene mkazi anaona kuti anasiya
copfunda cace m'dzanja lace, nathawira kubwalo, 14anaitana amuna a
m'nyumba yace, nanena ndi iwo kuti, Taonani, walowetsa kwa ife Mhebri kuti
atiseke ife, analowa kwa ine kugona ndi ine, ndipo ndinapfuula ndi mau
akuru: 15ndipo panali pamene iye anamva kuti ndinakweza mau anga ndi
kupfuula, iye anasiya copfunda cace kwa me nathawira kubwalo. 16Ndipo
anasunga copfunda cace cikhale ndi iye kufikira atabwera kwao
mbuyace. 17Ndipo ananena kwa iye monga mau awa, nati, Analowa kwa ine
kapolo wa Cihebri uja, munabwera naye kwathu, kundipunza ine: 18ndipo
panali pamene ndinakweza mau anga ndi kupfuula, iye anasiya cobvala cace
kwa ine, nathawira kunja. 19Ndipo panali pamene mbuyace anamva mau a
mkazi wace, amene ananena kwa iye, kuti, Coteroci anandicitira ine kapolo
wako; kuti iye anapsya mtima. 20Ndipo mbuyace wa Yosefe anamtenga iye
namuika m'kaidi, umo anamangidwa akaidi a mfumu: ndipo iye anali m'mwemo
m'kaidimo. 21Koma Yehova anali ndi Yosefe namcitira iye zokoma, nampatsa
ufulu pamaso pa woyang'anira kaidi. 22Ndipo woyang'anira kaidi anapereka
m'manja a Yosefe akaidi onse okhala m'kaidimo, ndipo zonse iwo anazicita
m'menemo, iye ndiye wozicita. 23Woyang'anira m'kaidi sanayang'anira kanthu
kali konse kamene kanali m'manja a Yosefe, cifukwa Yehova anali ndi iye; ndipo
zimene anazicita, Yehova anazipindulitsa.

Genesis 40

Yosefe m'kaidi amasulira maloto

1Ndipo panali zitapita izi, wopereka cikho wa mfumu ya Aigupto ndi wophika
mkate wace anamcimwira mbuye wao mfumu ya Aigupto. 2Ndipo Farao
anakwiyira akuru ace awiriwo wamkuru wa opereka cikho, ndi wamkuru wa
ophika mkate. 3Ndipo anaika iwo asungidwe m'nyumba ya kazembe wa alonda,
m'kaidi, umo anamangidwa Yosefe. 4Ndipo kazembe wa alonda anapereka iwo
kwa Yosefe, ndipo iye anawatumikira iwo: ndipo anakhala nthawi
mosungidwamo. 5Ndipo analota maloto onse awiri, yense lata lace, usiku
umodzi, yense monga mwa kumasulira kwa loto lace, wopereka cikho ndi
wophika mkate wa mfumu ya Aigupto, amene anamangidwa m'kaidi. 6Ndipo
Yosefe analowa kwa iwo m'mawa, nawaona iwo, taonani, anali oziya. 7Ndipo
anafunsa akuru a Farao osungidwa naye m'nyumba ya mbuyace, kuti, Nkhope
zanu zagwa bwanji lero? 8Ndipo iwo anati kwa iye, Ife talota maloto, ndipo tiribe
wotimasulira. Ndipo Yosefe anati kwa iwo, Kodi Mwini kumasulira si ndiye
Mulungu? Mundifotokozeretu. 9Ndipo wopereka cikho wamkuru anafotokozera
Yosefe loto lace, nati kwa iye, M'kulota kwanga, taona, mpesa unali pamaso
panga: 10ndipo m'mpesamo munali nthambi zitatu: ndipo unali wonga
unaphuka, ndipo maluwa ace anaphuka; nabala matsamvu ace mphesa
zakuca: 11ndipo cikho ca Farao cinali m'dzanjalanga: ndipo ndinatenga
mphesa, ndi kufinyira m'cikho ca Farao ndi kupereka cikho m'dzanja la
Farao. 12Ndipo Yosefe anati kwa iye, Mmasuliro wace ndi uwu: nthambi zitatu
ndizo masiku atatu; 13akali masiku atatu Farao adzatukula mutu wako,
nadzabwezera iwe nchito yako; ndipo udzapereka cikho ca Farao m'dzanja
lace, monga kale lomwe m'mene unali wopereka cikho cace. 14Koma
undikumbukire ine m'mene kudzakhala bwino ndi iwe, ndipoundicitiretu ine
kukoma mtima: nundichule ine kwa Farao, nunditurutse ine
m'nyumbamu: 15cifukwa kuti ndinabedwa ndithu m'dziko la Ahebri; ndiponso
pano sindinacite kanthu kakundiikira ine m'dzeniemu. 16Pamene wophika
mkate anaona kuti mmasuliro wace unali wabwino, iye anati kwa Yosefe, Inenso
ndinalimkulota, ndipo, taonani, malicero atatu a mikate yoyera anali pamtu
panga; 17m'licelo lapamwamba munali mikate ya Farao ya mitundu mitundu;
ndipo mbalame zinadya ya m'licelo la pamutu panga. 18Ndipo Yosefe
anayankha nati, Mmasuliro wace ndi uwu: malicelo atatu ndiwo masiku
atatu; 19akali masiku atatu Farao adzakweza mutu wako ndi kuucotsa,
nadzakupacika iwe pamtengo: ndipo mbalame zidzadya mnofu wako. 20Ndipo
panali tsiku lacitatu ndilo tsiku lakubadwa kwace kwa Farao, iye anakonzera
anyamata ace madyerero, ndipo anakweza mutu wa wopereka cikho wamkuru,
ndi mutu wa wophika mkate wamkuru pakati pa anyamata ace. 21Ndipo
anabwezanso wopereka cikho ku nchito yace; ndipo iye anapereka cikho
m'manja a Farao. 22Koma anampacika wophika mkate wamkuru; monga
Yosefe anawamasulira. 23Koma wopereka cikho wamkuru sanakumbukira
Yosefe, koma anamuiwala.

Genesis 41

Yosefe ammasulira Farao maloto ace

1Ndipo panali zitapita zaka ziwiri zamphumphu, Farao analota; ndipo, taonani, anaima panyanja. 2Ndipo, taonani, zinaturuka m'nyanja ng'ombe zazikazi zisanu ndi ziwiri za maonekedwe okoma ndi zonenepa; ndipo zinadya mabango. 3Ndipo, taonani ng'ombe zazikazi zisanu ndi ziwiri zinaturuka m'nyanjamo pambuyo pao, za maonekedwe oipa ndi zoonda; ndipo zinaima pa ng'ombe zinazo m'mphepete mwa nyanja. 4Ndipo ng'ombe zazikazi za maonekedwe oipa ndi zoonda zinadya ng'ombe zazikazi zisanu ndi ziwiri za maonekedwe abwino ndi zonenepazo. Ndipo Farao anauka. 5Ndipo anagona nalotanso kaciwiri: ndipo taonani, ngala zisanu ndi ziwiri za tirigu zinamera pa mbuwa imodzi, zonenepa ndi zabwino. 6Ndipo, taonani, ngala zisanu ndi ziwiri, zoonda zopsyerera ndi mphepo ya kum'mawa, zinamera pambuyo pao. 7Ndipo ngala zoondazo zinameza ngala zisanu ndi ziwiri zonenepa ndi zodzalazo. Ndipo Farao anauka, ndipo, taonani, analota. 8Ndipo panali m'mamawa mtima wace unabvutidwa; ndipo anatumiza naitana amatsenga onse a m'Aigupto, ndi anzeru onse a momwemo: ndipo Farao anafotokozera iwo loto lace; koma panalibe mmodzi anakhoza kuwamasulira iwo kwa Farao. 9Pamenepo wopereka cikho wamkuru anati kwa Farao, kuti, Ine ndidzakumbukira zocimwa zanga lero. 10Farao anakwiya ndi anyamata ace, nandiika ine ndisungidwe m'nyumba ya kazembe wa alonda, ine ndi wophika mkate wamkuru: 11ndipo tinalota loto usiku umodzi ine ndi iye; tinalota munthu yense monga mwa kumasulira kwa loto lace. 12Ndipo panali ndi ife mnyamata, Mhebri, kapolo wa kazembe wa alonda, ndipo ife tinafotokozera iye, ndipo iye anatimasulira ife maloto athu; kwa munthu yense monga mwa loto lace anatimasulira. 13Ndipo panali monga momwe iye anatimasulira, momwemo mudacitika; ine anandibwezera mu utumiki wanga, mnzanga anampacika. 14Ndipo Farao anatumiza nakaitana Yosefe; ndipo anamturutsa iye msanga m'dzenjemo: ndipo iye anameta, napindula malaya ace, nalowa kwa Farao. 15Farao ndipo anati kwa Yosefe, Ine ndalota loto, koma palibe wondimasulira; ndipo ndamva alikunena za iwe kuti, ukamva loto udziwa kumasulira. 16Ndipo Yosefe anayankha Farao kuti, Si mwa ine; koma Mulungu adzayankha Farao mwamtendere. 17Ndipo Farao ananena kwa Yosefe, M'loto langa taona, ndinaima m'mphepete mwa nyanja; 18ndipo taona, zinaturuka m'nyanjamo ng'ombe zazikazi zisanu ndi ziwiri, zonenepa ndi za maonekedwe abwino; ndipo zinadya m'mabango; 19ndipo, taona, ng'ombe zazikazi zisanu ndi ziwiri zina zinaturuka pambuyo pao zosauka ndi za maonekedwe oipa ndi zoonda, zoipa zotere sindinazione m'dziko la Aigupto; 20ndipo ng'ombe zazikazi zoonda ndi za maonekedwe oipa zinadya ng'ombe zazikazi zisanu ndi ziwiri zonenepa, 21Ndipo pamene zinadya sizinadziwika kuti zinadya; koma zinaipabe m'maonekedwe ao monga poyamba. 22Pamenepo ndinauka. Ndipo ndinaona m'kulota kwanga, taona, ngala zisanu ndi ziwiri zinamera pa mbuwa imodzi zodzala ndi zabwino; 23ndipo, taona, ngala zisanu ndi ziwiri zina zofota, zoonda, zopsyerera ndi mphepo ya kum'mawa, zinamera pambuyo pao; 24ndipo ngala zoonda zinameza ngala zisanu ndi ziwiri zabwino; ndipo ndinafotokozera amatsenga: koma panalibe wondimasulira ine. 25Ndipo Yosefe anati kwa Farao, Loto la Farao liri limodzi: cimene Mulungu ati acite

wammasulira Farao. 26Ng'ombe zazikazi zisanu ndi ziwiri zabwino ndizo zaka zisanu ndi ziwiri, ndi ngala zisanu ndi ziwiri zabwino ndizo zaka zisanu ndi ziwiri: loto liri limodzi. 27Ng'ombe zazikazi zisanu ndi ziwiri zoonda ndi za maonekedwe oipa zinaturuka pambuyo pao ndizo zaka zisanu ndi ziwiri, ndiponso ngala zisanu ndi ziwiri zopanda kanthu zopsyerera ndi mphepo ya kum'mawa, ndizo zaka zisanu ndi ziwiri za njala. 28Ici ndi cinthu cimene ndinena kwa Farao: cimene Mulungu ati acite wasonyeza kwa Farao. 29Taonani, zidzafika zaka zisanu ndi ziwiri zakucuruka cakudya m'dziko lonse la Aigupto; 30ndipo pambuyo pao zidzauka zaka zisanu ndi ziwiri za njala; ndipo anthu adzaiwala zocuruka zonsezo m'dziko la Aigupto; ndipo njala idzapululutsa dziko; 31ndipo zocuruka sizidzazindikirika cifukwa ca njala ikudza m'mbuyoyo, pakuti idzabvuta. 32Ndipo lotolo linabwezedwa kawiri kwa Farao, cifukwa cinthu ciri cokhazikika ndi Mulungu, ndipo Mulungu afulumira kucicita. 33Tsopano, Farao afunefune'munthu wakuzindikira ndi wanzeru, amkhazike iye ayang'anire dziko la Aigupto. 34Farao acite cotere, alembe woyang'anira dziko wosonkhetsa limodzi la magawo asanu la dziko la Aigupto m'zaka zisanu ndi ziwiri zakucuruka dzinthu. 35Iwo asonkhanitse cakudya conse ca zaka zabwino izo zirinkudzazo, aunjike tirigu m'manja a Farao akhale cakudya m'midzi, namsunge. 36Ndipocakudyacocidzakhalam'dziko cosonkhera zaka zisanu ndi ziwiri za njala imene idzakhala m'dziko la Aigupto; kuti dziko lisanonongedwe ndi njala.

Yosefe wolamulira dziko la Aigupto

37Ndipo cinthuco cinali cabwino m'maso mwa Farao, ndi m'maso mwa anyamata ace. 38Ndipo Farao anati kwa anyamata ace, Kodi ife tidzaone munthu ngati uyu, mzimu wa Mulungu uli m'mtima mwace? 39Ndipo Farao anati kwa Yosefe, Popeza Mulungu wakuonetsa iwe zonsezo palibe wina wakuzindikira ndi wanzeru ngati iwe. 40Uziyang'anira pa nyumba yanga, ndipo anthu anga onse adzalamulidwa mwa mau ako; pa mpando wacifumu pokha ine ndidzakuposa iwe. 41Ndipo Farao anati kwa Yosefe, Taona, ndakhazika iwe wolamulira dziko lonse la Aigupto. 42Ndipo Farao anacotsa mphete yosindikizira yace pa dzanja lace, naibveka pa dzanja la Yosefe, nambveka iye ndi zobvalira zabafuta, naika unyolo wagolidi pakhosi pace; 43ndipo anamkweza iye m'gareta wace waciwiri amene anali naye: ndipo anapfuula patsogolo pa iye, Gwadani; ndipo anamkhazika iye wolamulira dziko lonse la Aigupto, 44Ndipo Farao anati kwa Yosefe, Ine ndine Farao, ndipo popanda iwe palibe munthu ali yense adzatukula dzanja lace kapena mwendo wace m'dziko lonse la Aigupto. 45Ndipo Farao anamucha dzina la Yosefe Zafenati-Panea; ndipo anampatsa akwatire Asenati mwana wamkazi wa Potifera wansembe wa Oni. Ndipo Yosefe anaturuka wolamulira, nayendayenda m'dziko la Aigupto. 46Ndipo Yosefe anali wa zaka makumi atatu pamene iye anaima pamaso pa Farao mfumu ya Aigupto, Ndipo Yosefe anaturuka pamaso pa Farao, napitapita pa dziko lonse la Aigupto, 47Ndipo zaka zisanu ndi ziwiri zakucuruka dzinthu nthaka inabala zambirimbiri. 48Ndipo anasonkhanitsa cakudya conse ca zaka zisanu ndi ziwiri cimene cinali m'dziko la Aigupto, nasunga cakudyaco m'midzi; cakudya ca m'minda, yozinga midzi yonse, anacisunga m'menemo. 49Ndipo Yosefe anasunga tirigu ngati mcenga wa

panyanja, wambirimbiri kufikira analeka kuwerenga; cifukwa anali wosawerengeka. 50Ndipo kwa Yosefe anabadwa ana amuna awiri, cisanafike caka ca njala, amene Asenati mwana wamkazi wa Porifera wansembe wa Oni anambalira iye. 51Ndipo Yosefe anamucha dzina la woyamba Manase, cifukwa anati iye, Mulungu wandiiwalitsa ine zobvuta zanga zonse, ndi nyumba yonse ya atate wanga. 52Ndipo dzina la waciwiri anamucha Efraimu: cifukwa Mulungu anandibalitsa ine m'dziko la kusauka kwanga. 53Ndipo zaka zakucuruka dzinthu zisanu ndi ziwiri za m'dziko la Aigupto, zinatha. 54Ndipo zinayamba kufika zaka zisanu ndi ziwiri za njala, monga ananena Yosefe; ndipo munali njala m'maiko monse; koma m'dziko lonse la Aigupto munali cakudya. 55Ndipo pamene dziko lonse la Aigupto linali ndi njala, anthu anapfuulira Farao awapatse cakudya; ndipo Farao anati kwa Aaigupto onse, Pitani kwa Yosefe: cimene iye anena kwa inu citani. 56Ndipo njala inali pa dziko lonse lapansi; ndipo Yosefe anatsegula nkhokwe zonse nagulitsa Aaigupto: ndipo njala inakula m'dziko la Aigupto. 57Ndipo maiko onse anafika ku Aigupto kudzagula tirigu kwa Yosefe: cifukwa njala inakula m'dziko lonse lapansi.

Genesis 42

Abale a Yosefe afika ku Aigupto

1Ndipo anaona Yakobo kuti m'Aigupto munali tirigu, nati Yakobo kwa ana ace
amuna, Cifukwa canji mulinkuyang'anana? 2Ndipo iye anati, Taonani, ndamva
kuti m'Aigupto muli tirigu, mutsikireko mutigulire kumeneko; kuti tikhale ndi
moyo, tisafe. 3Ndipo abale ace a Yosefe khumi anatsikira kukagula tirigu
m'Aigupto. 4Koma Yakobo sanamtuma Benjamini mphwace wa Yosefe,
pamodzi ndi abale ace, cifukwa anati, Coipa cingamgwere iye. 5Ndipo ana
amuna a Israyeli anadza kudzagula mwa iwo amene anadzako, pakuti m'dziko
la Kanani munali njala. 6Ndipo Yosefe anali wolamulira dziko; ndiye amene
anagulitsa kwa anthu onse a m'dziko; ndipo anafika abale ace a Yosefe,
namweramira pansi, nkhope zao pansi. 7Ndipo Yosefe anaona abale ace, ndipo
anazindikira iwo, koma anadziyesetsa kwa iwo ngati mlendo, nanena kwa iwo
mwankhanza: ndipo anati kwa iwo, Mufuma kuti inu? nati iwo, Ku dziko la
Kanani kudzagula cakudya. 8Ndipo Yosefe anazindikira abale ace, koma iwo
sanamzindikira iye. 9Ndipo Yosefe anakumbukira maloto amene analoto za iwo,
ndipo anati kwa iwo, Ozonda inu; mwadzera kudzaona usiwa wa
dziko. 10Ndipo iwo anati kwa iye, Iai, mbuyanga, koma akapolo anu adzera
kudzagula cakudya. 11Tonse tiri ana amuna a munthu mmodzi; tiri oona,
akapolo anu, sitiri ozonda. 12Ndipo iye anati kwa iwo, Iai, koma mwadzera kuti
muone usiwa wa dziko. 13Nati iwo, Akapolo anu ndife abale khumi, ana amuna
a munthu mmodzi m'dziko la Kanani; ndipo, taonani, wamng'ono ali ndi atate
wathu lero; ndipo palibe mmodzi. 14Ndipo Yosefe anati kwa iwo, dico cimene
ndinakunenani inu, kuti, Ndinu ozonda. 15Mudzayesedwa ndi ici, pali moyo wa
Farao, simudzaturuka muno, koma akadze kuno mphwanu ndiko. 16Tumizani
mmodzi wa inu akatenge, adze naye mphwanu: ndipo inu mudzamangidwa kuti
mau anu ayesedwe, ngati zoona ziri mwa inu: penatu, pali moyo wa Farao, muli
ozonda ndithu. 17Ndipo anaika onse m'kaidi masiku atatu. 18Ndipo Yosefe
anati kwa iwo tsiku lacitatu, Citani ici, kuti mukhale ndi moyo; ine ndiopa
Mulungu; 19ngati muli oona, mmodzi wa abale anu amangidwe m'kaidi
momwemo; mukani inu, mupite naye tirigu wa njala ya mabanja anu; 20koma
mukatenge mphwanu kudza naye kwa ine, kuti atsimikizidwe mau anu ndipo
simudzafa. Ndipo anacita comweco. 21Ndipo iwo anati wina ndi mnzace,
Tacimwiratu mbale wathu, pamene tinaona kubvutidwa kwa mtima wace,
potipembedzera ife, koma ife tinakana kumvera, cifukwa cace kubvutidwa
kumene kwatifikira. 22Ndipo Rubeni anayankha nati kwa iwo, Kodi sindinanena
kwa inu kuti, Musacimwire mwanayu; ndipo inu munakana kumvera? cifukwa
cacenso, taonani mwazi wace ufunidwa. 23Ndipo sanadziwa kuti, Yosefe
anamva; cifukwa anali ndi womasulira. 24Ndipo anawafotokozera iwo nalira,
nawatembenukiranso, nanena nao, nampatula Simeoni mwa iwo, nammanga
iye pamaso pao. 25Ndipo Yosefe analamulira kuti adzaze zotengera zao ndi
tirigu, ndi kubweza ndalama zao, ali yense m'thumba mwace, ndi kuwapatsa
phoso la panjira; ndipo anatero nao.

Abale a Yosefe apita kwao

26Ndipo anasenzetsa aburu ao tirigu wao nacokapo. 27Ndipo pamene wina wa
iwo anamasula thumba lace kuti adyetse buru wace pacigono, anapeza
ndalama zace; taonani, zinali kukamwa kwa thumba lace. 28Ndipo iye anati

kwa abale ace, Wandibwezera ine ndalama zanga, taonani, ziri kukamwa kwa thumba langa; ndipo mitima yao inawadera iwo, nanthunthumira, natembenukirana wina ndi mnzace kuti, Nciani ici Mulungu waticitira ife? 29Ndipo anadza kwa Yakobo atate wao ku dziko la Kanani, namfotokozera iye zonse zinaonekera kwa iwo; 30kuti, Munthu mwini dziko, ananena ndi ife mwankharwe, natiyesa ife ozonda dziko. 31Koma ife tinati kwa iye, Tiru anthu oona; sitiri ozonda; 32tiri abale khumi ndi awiri, ana a atate wathu; wina palibe, ndipo lero wamng'ono ali ndi atate wathu m'dziko la Kanani. 33Ndipo munthuyo mwini dziko anati kwa ife, Momwemu ndidzadziwa kuti muli anthu oona; siyani mmodzi wa abale anu pamodzi ndi ine, tengani tirigu wa njala ya kwanu, mukani; 34idzani naye mphwanu kwa ine, ndipo ndidzadziwa kuti simuli ozonda koma anthu oona: comweco ndidzakubwezerani inu mbale wanu, ndipo mudzacita malonda m'dziko muno. 35Ndipo panali pamene analikukhuthula matumba ao, taonani, phukusi la ndalama la yense linali m'thumba lace; ndipo pamene iwo ndi atate ao anaona mapukusi a ndalama anaopa, 36Ndipo Yakobo atate wao anati kwa iwo, Munandilanda ine ana; Yosefe palibe, Simeoni palibe, ndipo mudzacotsa Benjamini: zonse zimene zandigwera. 37Ndipo Rubeni anati kwa atate wace, kuti, Muwaphe ana anga amuna awiri ndikapanda kumbweza iye kwa inu; mumpereke iye m'manja mwanga, ndipo ine ndidzambwezanso kwa inu. 38Ndipo iye anati, Mwana wanga sadzatsikira ndi inu, cifukwa kuti mkuru wace wafa, ndipo watsala iye yekha; ngati coipa cikamgwera iye m'njira m'mene mupitamo, inu mudzatsitsira ndi cisoni imvi zanga kumanda.

Genesis 43

Abale a Yosefe atsikiranso ku Aigupto

1Ndipo njala inakula m'dzikomo. 2Ndipo panali pamene atatha kudya tirigu
yense anatengayo ku Aigupto atate wao anati kwa iwo, Pitaninso, mukatigulire
ife cakudya pang'ono. 3Ndipo Yuda ananena ndi iye kuti, Munthu uja
anatilimbitsira mau kuti, Simudzaonanso nkhope yanga, koma mphwanu akhale
ndi inu ndiko. 4Ngati mudzatuma mphwathu pamodzi ndi ife, tidzatsikira ndi
kugulira inu cakudya. 5Koma mukapanda kumtuma iye sititsika; pakuti munthu
uja anati kwa ife, Simudzaona nkhope yanga, ngati mphwanu sali ndi
inu. 6Ndipo Israyeli anati, Cifukwa ninji munandicitira ine coipa cotero kuti
munamuuza munthuyo muli ndi mphwanu? 7Ndipo iwo anati, Munthuyo
anafunsitsa za ife, ndi za abale athu, kuti, Atate wanu alipo? Kodi muli ndi
mphwanu? ndipo tinamfotokozera iye monga mwa mau amenewo: ngati
tinadziwa kuti iye adzati, Idzani naye mphwanu? 8Ndipo Yuda anati kwa atate
wace Israyeli, Mumtume mnyamata pamodzi ndi ine ndipo ife tidzanyamuka ndi
kupita; kuti tikhale ndi moyo tisafe, ife ndi inu ndi ana athu ang'ono. 9Ine
ndidzakhala cikole, pa manja anga mudzamfunsa: ndikapanda kumbwezera
kwa inu ndi kumuimitsa pamaso panu, cifukwa cace cidzakhala pa ine masiku
onse: 10pakuti tikadaleka kucedwa mwenzi tsopano titabwera kawiri. 11Ndipo
Israyeli atate wao anati kwa iwo, Ngati comweco tsopano citani ici: tengani
zipatso za m'dziko muno m'zotengera zanu, mumtengere munthu uja mphatso,
mafuta a mankhwala pang'ono, ndi uci pang'ono, zonunkhira ndi mure, ndi
mfula, ndi katungurume; 12nimutenge ndalama zowirikiza m'manja mwanu;
ndipo ndalama zimene zinabwezedwa kukamwa kwa matumba anu
mutengenso m'manja mwanu; kapena sanacita dala; 13mutengenso mphwanu,
nimuoyamuke, mupitenso kwa munthu uja: 14Mulungu Wamphamvuyonse
adzakupatsani inu cifundo pamaso pa munthu uja, kuti akumasulireni inu mbale
wanu wina ndi Benjamini. Ndipo ine, ngati ndikhala wopanda ana, ndikhalatu.

Abalewo m'nyumba Ya Yosefe

15Amunawo ndipo anatenga mphatso, natenga ndalama zowirikiza m'manja
mwao, ndi Benjamini; ndipo ananyamuka ndi kutsikira ku Aigupto, naima
pamaso pa Yosefe. 16Ndipo pamene anaona Benjamini pamodzi nao, anati
kwa tsanyumba wace, Lowa nao anthuwo m'nyumba, kaphere iwo, kakoozere,
cifukwa anthuwo adzadya ndi ine usana uno. 17Munthuyo anacita monga
anamuuza Yosefe, ndipo munthuyo analowa nao anthuwo m'nyumba ya
Yosefe. 18Anthuwo ndipo anaopa, cifukwa analowezedwa m'nyumba ya
Yosefe; nati, Cifukwa ca ndalama zila zinabwezedwa m'matumba athu nthawi
yoyamba ija, ife tilowezedwa, kuti aone cifukwa ndi ife, atigwere ife, atiyese ife
akapolo, ndi aburu athu. 19Ndipo anayandikira kwa tsanyumba wa Yosefe,
ndipo ananena ndi iye pa khomo la nyumba, nati, 20Mfumu, tinatsikira ndithu
nthawi yoyamba kudzagula cakudya: 21ndipo panali pamene ife tinafika
padgono, tinamasula matumba athu, ndipo taonani ndalama za yense zinali
kukamwa kwa thumba lace, ndalama zathu mkulemera kwace; ndipo tabwera
nazo m'manja mwathu. 22Ndalama zina tatenga m'manja mwathu kuti tigule
cakudya: sitimdziwa amene anaika ndalama zathu m'matumba athu. 23Ndipo
iye anati, Mtendere ukhale ndi inu, musaope; Mulungu wanu, ndi Mulungu wa
atate wanu anakupatsani inu cum a m'matumba anu; ine ndinali nazo ndalama

zanu. Pamenepo anawaturutsira Simeoni. 24Ndipo munthuyo analowetsa anthu m'nyumba ya Yosefe, nawapatsa iwo madzi, natsuka mapazi ao, napatsa aburu ao cakudya. 25Ndipo anakonzeratu mphatso asanafike Yosefe usana; cifukwa anamva kuti adzadya cakudya pamenepo. 26Pamene Yosefe anadza kunyumba kwace, analowa nazo m'nyumba mphatso zinali m'manja mwao, namweramira iye pansi. 27Ndipo anafunsa iwo za ubwino wao, nati, Kodi atate wanu ali ndi moyo? wokalamba uja amene nunanena uja: kodi alipo? 28Ndipo iwo anati, Kapolo wanu atate wathu ili bwino, alipo. Ndipo anawerama, namgwadira iye. 29Ndipo iye anatucula maso ace naona Benjamini mphwace, mwana wa amace, nati, Kodi uyu ndi mphwanu wamng'ono uja, amene munanena ndi ine uja? Ndipo iye anati, Mulungu akucitire we ufulu, mwana wanga. 30Ndipo Yosefe anafulumira, cifukwa mtima wace unakhumbitsa mphwace, ndipo mafuna polirira; nalowa m'cipinda ace naliramo. 31Ndipo anasamba ikhope yace, naturuka; ndipo anadziletsa, nati, Ikani cakudya. 32Ndipo anamuikira iye cace pa yekha, ndi wo cao pa okha, ndi Aaigupto ikudya naye cao pa okha; cifukwa aigupto sanathei kudya cakudya pamodzi ndi Ahebri: cifukwa kucita comweco nkunyansira Aaigupto. 33Ndipo anakhala pamaso pace, woyanba monga ukuru wace, ndi wanng'ono mensa ung'ono wace; ndipo mazizwa wina ndi wina. 34Ndipo mawagawira mitanda ya patsogolo pace; koma mtanda wa Benjamini maposa mitanda ya onsewo kasanu. Ndipo anamwa, nasekera pamodzi ndi iye.

Genesis 44

Abalewo ayesedwa ndi Yosefe

1Ndipo Yosefe anauza tsanyumba wace kuti, Dzaza matumba a anthuwo ndi
cakudya, monga angathe kunyamula, ndi kuika ndalama za yense kukamwa
kwa thumba lace. 2Nuike cikho canga, cikho casiliva ciija, kukamwa kwa
thumba la wamng'ono, pamodzi ndi ndalama za tirigu zace. Ndipo iye anacita
monga mau ananena Yosefe. 3Pamene kudaca, anamukitsa anthu iwo ndi
aburu ao. 4Ataturuka m'mudzi asanamuke patari, Yosefe anati kwa tsanyumba
wace, Tanyamuka, talondola anthu aja, ukawapeza unene nao, Cifukwa canji
mwabwezera zoipa m'malo mwa zabwino? 5Kodi si ndico comwera naco
mbuyanga, naombeza ula naco? Mwacitira coipa pakutero. 6Ndipo anapeza
iwo, nanena nao mau omwewo. 7Nati kwa iye, Bwanji mbuyanga anena mau
otere? Ngati nkutheka kuti akapolo anu acite cotero? 8Taonani, ndalama zija,
tinazipeza kukamwa kwa matumba athu, tinazibwezanso kwa inu kuturuka
m'dziko la Kanani; nanga bwanji tingabe m'nyumba ya mbuyanga kapena siliva
kapena golidi? 9iye wa akapolo anu ampeza naco afe, ndipo ifenso tidzakhala
akapolo a mbuyanga. 10Ndipo iye mati, Tsononso cikhale monga mwa nau anu:
iye amene ampeza naco adzakhala kapolo wanga; ndipo inu nudzakhala
opanda cifukwa. 11Ndipo anafulumira natsitsa pansi zense thumba lace,
namasula yense humba lace. 12Ndipo iye anafunauna kuyambira pa wamkuru
naleka pa wamng'ono; nacipeza cikho n'thumba la Benjamini: 13ndipo
anang'amba zobvala zao, nasenzetsa yense buru wace, nabwera
kumuzi. 14Yudanso ndi abale ace anadza cu nyumba ya Yosefe; ndipo iye ikali
pamenepo; ndipo anagwa oansi patsogolo pace. 15Ndipo losefe anati kwa iwo,
Ici nciani nwacicita? Kodi simudziwa kuti nunthu ngati ine ndingathe kuzindidra
ndithu?

Yuda apembedzera Benjamini kwa Yosefe

16Ndico Yuda anati, Kodi tidzati bwanji kwa mbuyanga? kodi tidzanenanji?
kapena tidzawiringula ife bwanji? Mulungu wapeza mphulupulu ya akapolo anu;
taonani, tiri akapolo a mbuyanga, ife ndi iye amene anampeza naco cikho
m'dzanja lace. 17Ndipo iye anati, Ngati kutheka kuti ndicite cotero! Munthu
amene anampeza naco m'dzanja lace adzakhala kapolo wanga: koma inu,
kazipitani ndi mtendere kwa atate wanu.

18Ndipo Yuda anayandikira kwa iye nati, Mfumu, kapolo wanu aneneretu
m'makutu a mbuyanga, mtima wanu usapse pokwiya ndi kapolo wanu; cifukwa
muli ngati Farao. 19Mbuyanga anafunsa akapolo ace kuti, Kodi muli ndi atate
wanu kapena mbale wanu? 20Ndipo tinati kwa mbuyanga, Tiri ndi atate,
munthu wokalamba, ndi mwana wa ukalamba wace wamng'ono; mbale wace
wafa, ndipo iye yekha watsala wa amace, ndipo atate wace amkonda
iye. 21Ndipo munati kwa akapolo anu, Munditengere iye, kuti ndimuone iye
m'maso mwanga. 22Ndipo ife tinati kwa mbuyanga, Mnyamata sangathei
kumsiya atate wace; pakuti akamsiya atate wace, atate wace adzafa. 23Ndipo
munati kwa akapolo anu, Koma ngati mbale wanu safika pamodzi ndi inu,
simudzaonanso konse nkhope yanga, 24Ndipo panali titakwera kunka kwa
kapolo wanus atate, wanga, tinamfotokozera iye mau a mbuyanga. 25Ndipo
atate wathu anati, Mupitenso mutigulire ife cakudya pang'ono. 26Ndipo ife tinati,
Sitingathe kupita; mphwathu wamng'ono akakhala ndi ife, pamenepo tidzapita;

pakuti sitingaone nkhope ya munthu uja, mphwathu wamng'ono akapanda kukhala ndi ife. 27Ndipo kapolo wanu atate wanga anati kwa ife, Inu mudziwa kuti mkazi wanga anandibalira ine ana amuna awiri; 28wina anaturuka kwa ine ndipo ndinati, Zoonatu, wakadzulidwa; ndipo sindidzamuonanso iye; 29ndipo ngati mukandicotsera ameneyonso, ndipo ngati cimgwera coipa, mudzanditsitsira ndi cisoni imvi zanga kumanda. 30Cifukwa cace ndikafika kwa kapolo wanu atate wanga, ndipo mnyamata akapanda kukhala ndi ife; popeza moyo wace uli womangidwa ndi moyo wa mnyamatayo; 31kudzakhala pakuona kuti mnyamatayo palibe, adzafa; ndipo akapolo anu adzamtsitsira ndi cisoni imvi za atate wathu kumanda. 32Pakuti kapolo wanu anadziyesa cikole ca mnyamata pa atate wanga, kuti, Ndikapanda kumbwezeranso kwa inu, pamenepo ndidzakhala ndi cifukwa kwa atate wanga nthawi zonse. 33Tsopanotu, mtumiki wanu akhale kapolo wa mbuyanga m'malo mwa mnyamata; mnyamatayo akwere pamodzi ndi abale ace. 34Pakuti ndidzakwera bwanji kwa atate wanga, mnyamatayo akapanda kukhala ndi ine? ndingaone coipa cidzagwera atate wanga.

Genesis 45

Yosefe adziulula kwa abale ace

1Ndipo Yosefe sanakhoza kudziletsa pamaso pa onse amene anaima naye:
nati, Turutsa anthu onse pamaso panga. Ndipo panalibe munthu pamodzi ndi
iye pamene Yosefe anadziululira yekha kwa abale ace. 2Ndipo analira
momveka, ndipo anamva Aaigupto, ndipo anamva a m'nyumba ya
Farao. 3Ndipo Yosefe anati kwa abale ace, Ine ndine Yosefe; kodi-akali ndi
moyo atate wanga? Ndipo abale ace sanakhoza kumyankha iye; pakuti
anabvutidwa pakumuona iye. 4Ndipo Yosefe anati kwa abale ace,
Muyandikiretu kwa ine; nayandikira. Ndipo iye anati, Ine ndine Yosefe mbale
wanu, ine ndemwe munandigulitsa ndilowe m'Aigupto. 5Tsopano
musaphwetekwe mtima, musadzikwiyira inu nokha, kuti munandigulitsira ine
kuno, pakuti Mulungu ananditumiza ine patsogolo panu kuti ndisunge
moyo. 6Zaka ziwirizi muli njala m'dziko muno; ndipo zatsala zaka zisanu,
zopanda kulima kapena kusenga, 7Ndipo Mulungu anatumiza ine patsogolo
panu kuti ndikhazike inu mutsale m'dziko lapansi, ndi kusunga inu amoyo ndi
cipulumutso cacikuru. 8Ndipo tsopano sindinu amene munanditumiza ine
ndifike kuno, koma Mulungu, ndipo anandiyesa ine atate wa Farao, ndi mwini
banja lace lonse, ndi wolamulira dziko lonse la Aigupto. 9Fulumirani, kwerani
kunka kwa atate wanga, muti kwa iye, Cotere ati Yosefe mwana wanu, Mulungu
wandiyesa ine mwini Aigupto lonse: tsikirani kwa ine, musacedwe. 10Ndipo
mudzakhala m'dziko la Goseni, mudzakhala pafupi ndi ine, inu ndi ana anu, ndi
ana a ana anu, ndi nkhosa zanu, ndi zoweta zanu, ndi zonse muli
nazo; 11ndipo ndidzacereza inu komweko; pakuti zatsala zaka zisanu za njala;
kuti mungafikire umphawi, inu ndi banja lanu, ndi onse muli nao. 12Taonani,
maso anu aona, ndi maso a mphwanga Benjamini, kuti ndi m'kamwa mwanga
ndirikulankhula ndi inu. 13Ndipo mudzafotokozera atate wanga za ulemerero
wanga wonse m'Aigupto, ndi zonse mwaziona; ndipo muzifulumira ndi kutsitsira
kuno atate wanga. 14Ndipo anagwa pakhosi pace pa Benjamini, nalira; ndipo
Benjamini nalira pakhosi pace. 15Ndipo anampsompsona abale ace onse,
nalilira iwo; ndipo pambuyo pace abale ace onse anaceza naye.
16Ndipo mbiri yace inamveka m'nyumba ya Farao, kuti abale ace a Yosefe
afika; ndipo inamkomera Farao, ndi anyamata ace. 17Ndipo Farao anati kwa
Yosefe, Nena ndi abale ako, Citani ici; senzetsani nyama zanu, ndi kupita kunka
ku dziko la Kanani; 18katengeni atate wanu ndi mabanja anu, nimudze kwa ine;
ndipo ndidzakupatsani inu zabwino za dziko la Aigupto, ndipo mudzadya
zonenepa za dzikoli. 19Tsopano mwalamulidwa citani ici; muwatengere ana anu
ndi akazi magareta a m'dziko la Aigupto; nimubwere naye atate
wanu. 20Musasamalire cuma canu; popeza zabwino za dziko lonse la Aigupto
ndi zanu. 21Ndipo ana a Israyeli anacita cotero: ndipo Yosefe anawapatsa iwo
magareta monga analamulira Farao, nawapatsa phoso la panjira, 22Onse
anawapatsa yense zobvala zopindula; koma Benjamini anampatsa ndalama
zasiliva mazana atatu ndi zobvala zopindula zisanu. 23Kwa atate wace
anatumiza zotere: aburu khumi osenza zinthu zabwino za m'Aigupto, ndi aburu
akazi khumi osenza tirigu, ndi cakudya, ndi phoso la atate la panjira. 24Ndipo
anamukitsa abale ace, ndipo anacoka; ndipo anati kwa iwo, Musakangane
panjira. 25Ndipo anakwera kuturuka m'Aigupto, nafika ku dziko la Kanani kwa

Yakobo atate wao. 26Ndipo anamfotokozera iye kuti, Yosefe akali ndi moyo, ndipo alamulira m'dziko lonse la Aigupto, Pamenepo mtima wace unakomoka, pakuti sanawakhulupirira iwo. 27Ndipo anamfotokozera iye mau onse a Yosefe amene ananena ndi iwo; ndipo pamene anaona magareta amene Yosefe anatumiza kuti amtengeremo, mtima wa Yakobo atate wao unatsitsimuka; 28ndipo Israyeli anati, Cakwana; Yosefe mwana wanga akali ndi moyo; ndidzamuka ndikamuone iye ndisanafe.

Genesis 46

Yakobo atsikira ku Aigupto

1Ndipo Israyeli anamuka ulendo wace ndi zonse anali nazo, nafika ku
Beereseba, napereka nsembe kwa Mulungu wa Isake atate wace. 2Ndipo
Mulungu ananena kwa Israyeli, m'masomphenya a usiku, nati, Yakobo,
Yakobo. 3Nati iye, Ndine pano. Ndipo anati, Ine ndine Mulungu, Mulungu wa
atate wako; usaope kunka ku Aigupto; pakuti pamenepo ndidzakusandutsa iwe
mtundu waukuru; 4Ine ndidzatsikira pamodzi ndi iwe ku Aigupto; ndipo Ine
ndidzakubwezanso ndithu; ndipo Yosefe adzaika dzanja lace pamaso
pako. 5Ndipo Yakobo anacoka ku Beereseba, ndipo ana amuna a Israyeli
anamnyamula Yakobo atate wao, ndi ana ao ang'ono, ndi akazi ao, m'magareta
amene Farao anatumiza kuti amnyamule iye, 6Ndipo anatenga ng'ombe zao
ndi cuma cao anacipezam'dziko la Kanani, nadza ku Aigupto, Yakobo ndi mbeu
zace zonse pamodzi ndi iye; 7ana ace amuna, ndi zidzukulu zace zazimuna,
ndi ana akazi ace, ndi zidzukulu zace zazikazi, ndi mbeu zace zonse anadza
nazo m'Aigupto.

8Maina a ana a Israyeli amene anadza m'Aigupto ndi awa: Yakobo ndi ana
amuna ace: Rubeni mwana wamwamuna woyamba wa Yakobo. 9Ndi ana
amuna a Ruberu Hanoki, ndi Palu, ndi Hezroni, ndi Karmi. 10Ndi ana amuna a
Simeoni: Yemueli ndi Yamini, ndi Ohadi, ndi Yakini, ndi Zohari, ndi Sauli, mwana
wamwamuna wa mkazi wa ku Kanani. 11Ndi ana amuna a Levi: Gerisoni,
Kohati, ndi Merai. 12Ndi ana amuna a Yuda: Eri, ndi Onani, ndi Sela, ndi Perezi,
ndi Zera; koma Eri ndi Onani anafa m'dziko la Kanani. Ndi ana amuna a Perezi
ndiwo Hezroni ndi Hamuli. 13Ndi ana amuna a Isakara: Tola ndi Puva, ndi Yabi,
ndi Simroni. 14Ndi ana amuna a Zebuloni: Seredi, ndi Eloni ndi
Yaledi. 15Amenewo ndi ana amuna a Leya, amene anambalira Yakobo
m'Padanaramu, pamodzi ndi mwana wamkazi wace Dina; ana amuna ndi akazi
onse: ndiwo anthu makumi atatu kudza atatu. 16Ndi ana amuna a Gadi: Zifioni,
ndi Hagi, ndi Suni, ndi Ezboni, ndi Eri, ndi Arodi, ndi Areli. 17Ndi ana amuna a
Aseri: Yimna, ndi Yisiva, ndi Yisivi, ndi Beriya, ndi Sera mlongo wao; ndi ana a
Beriya: Hebere, ndi Maliki eli. 18Amenewa ndi ana a Zilipa, amene Labani
anampatsa Leya mwana wace wamkazi, amenewo anambalira Yakobo, anthu
khumi ndi asanu ndi mmodzi. 19Ana a Rakele mkazi wace wa Yakobo: Yosefe
ndi Benjamini. 20Kwa Yosefe kunabadwa m'dziko la Aigupto Manase ndi
Efraimu, amene Asenati mwana wamkazi wa Potifera wansembe wa Oni
anambalira iye. 21Ndi ana amuna a Benjamini: Bela ndi Bekeri, ndi Asibeli, ndi
Gera, ndi Namani, ndi Ehi ndi Rosi, Mupimu ndi Hupimu, ndi Aridi. 22Amenewo
ndi ana a Rakele, amene anabadwira Yakobo; anthu onse ndiwo khumi ndi
anai. 23Ndi ana amuna a Dani: Husimu. 24Ndi ana amuna a Nafitali: Yazeeli,
ndi Guni, ndi Yezera ndi Silemu. 25Amenewa ndi ana a Biliha, amene Labani
anampatsa Rakele mwana wace wamkazi, amenewo anambalira Yakobo; anthu
onse ndiwo asanu ndi awiri. 26Ndi anthu onse amene anadza ndi Yakobo
m'Aigupto, amene anaturuka m'cuuno mwace, pamodzi ndi akazi a ana amuna
a Yakobo ndiwo makumi asanu ndi limodzi kudza asanu ndi mmodzi; 27ndi ana
amuna a Yosefe, amene anambadwira iye m'Aigupto ndiwo anthu awiri; anthu
onse a mbumba ya Yakobo, amene analowa m'Aigupto anali makumi asanu ndi
awiri.

Yakobo akomana ndi Yosefe

28Ndipo anatumiza Yuda patsogolo pace kwa Yosefe, amtsogolere kumuonetsa
njira yomka ku Goseni: ndipo anafika ku dziko la Goseni. 29Ndipo Yosefe
anamanga gareta lace nakwera kunka kukakomana naye Israyeli atate wace,
ku Goseni, ndipo anadzionetsera yekha kwa iye, nagwera pakhosi pace
nakhala m'kulira pakhosi pace. 30Ndipo Israyeli anati kwa Yosefe, Ndife
tsopano, popeza ndaona nkhope yako, kuti ukali ndi moyo. 31Ndipo Yosefe
anati kwa abale ace, ndi kwa mbumba ya atate wace, Ndidzanka, ndikauze
Farao, ndipo ndidzati kwa iye, Abale anga ndi mbumba ya atate wanga, amene
anali m'dziko la Kanani, afika kwa ine; 32ndipo anthuwo ali abusa cifukwa
anakhala oweta ng'ombe; ndipo anadza ndi nkhosa zao ndi ng'ombe zao ndi
zonse ali nazo. 33Ndipo padzakhala pamene Farao adzaitana inu, nadzati,
Nchito yanu njotani? 34mudzati, Akapolo anu akhala oweta ng'ombe ciyambire
ubwana wathu kufikira tsopano, ife ndi atate athu; kuti mukhale m'dziko la
Goseni; a cifukwa abusa onse anyansira Aaigupto.

Genesis 47

Yakobo aonetsedwa kwa Farao

1Ndipo Yosefe analowa nauza Farao nati, Atate wanga ndi abale anga, ndi
nkhosa zao ndi ng'ombe zao, ndi zonse ali nazo, anacokera ku dziko la Kanani;
ndipo, taonani, ali m'dziko la Goseni. 2Ndipo mwa abale ace anatengako anthu
asanu, nawaonetsa iwo kwa Farao. 3Ndipo Farao anati kwa abale ace, Nchito
yanu njotani? ndipo iwo anati kwa Farao, Akapolo anu ndi abusa, ife ndi atate
athu. 4Nati kwa Farao, Tafika kuti tikhale m'dzikomo; popeza palibe podyetsa
zoweta za akapolo anu; pakuti njala yakula m'dziko la Kanani. Mulole tsopano
akapolo anu akhale m'dziko la Goseni. 5Ndipo Farao anati kwa Yosefe, Atate
wako ndi abale ako afika kwa iwe; 6dziko la Aigupto liri pamaso pako:
uwakhazike atate wako ndi abale ako pa dera lokometsetsa la dziko; akhale
m'dziko la Goseni; ndipo ngati udziwa anthu anzeru a mwa iwo, uwaike iwo
ayang'anire ng'ombe zanga. 7Ndipo Yosefe analowa naye Yakobo atate wace,
namuika iye pamaso pa Farao; ndipo Yakobo anamdalitsa Farao. 8Ndipo Farao
anati kwa Yakobo, Masiku a zaka za moyo wanu ndi angati? 9Ndipo Yakobo
anati kwa Farao, Masiku a zaka za ulendo wanga ndi zaka zana limodzi kudza
makumi atatu; masiku a zaka za moyo wanga ali owerengeka ndi oipa,
sanafikire masiku a zaka za moyo wa makolo angam'masikua
ulendowao. 10Ndipo Yakobo anamdalitsa Farao, naturuka pamaso pa
Farao. 11Ndipo Yosefe anakhazika atate wace ndi abale ace, napatsa iwo
pokhala m'dziko la Aigupto, m'dera lokometsetsa la m'dziko, m'dziko la
Ramese, monga analamulira Farao. 12Ndipo Yosefe anacereza atate wace ndi
abale ace, ndi mbumba yonse ya atate wace ndi cakudya monga mwa mabanja
ao.

Yosefe agulira Farao dziko la Aigupto

13Ndipo munalibe cakudya m'dziko lonse; pakuti njala inalimba kwambiri;
cifukwa cace dziko la Aaigupto ndi dziko la Kanani unalefuka cifukwa ca
njalayo. 14Ndipo Yosefe anasonkhanitsa ndalama zonse anazipeza m'dziko la
Aigupto ndi m'dziko la Kanani, za tirigu amene anagula; ndipo Yosefe
anapereka ndalama ku nyumba ya Farao. 15Ndipo zitatha ndalama zonse
m'dziko la Aigupto ndi m'dziko la Kanani, Aaigupto onse anadza kwa Yosefe,
nati, Mutipatse ife cakudya; tiferenji pamaso panu? zatsirizika
ndalama. 16Ndipo Yosefe anati, Mundipatse ng'ombe zanu: ndipo
ndidzakupatsani inu mtengo wa ng'ombe zanu ngati ndalama
zatsirizika. 17Ndipo anadza nazo ng'ombe zao kwa Yosefe, ndipo Yosefe
anapatsa iwo cakudya cosinthana ndi akavalo, ndi nkhosa, ndi ng'ombe, ndi
aburu; ndipo anawadyetsa iwo ndi cakudya cosinthana ndi zoweta zao zonse
caka cimeneco. 18Citatha caka cimeneco, anadza kwa iye caka caciwiri, nati
kwa iye, Sitibisira mbuyathu kuti ndalama zathu zonse zatha; ndipo zoweta za
ng'ombe oza mbuyathu: palibe kanthu kotsala pamaso pa mbuyathu, koma
matupi athu ndi maiko athu; 19tiferenji pamaso panu, ife ndi dziko lathu?
mutigule ife ndi dziko lathu ndi cakudya, ndipo ife ndi dziko lathu tidzakhala
akapolo a Farao; ndipo mutipatse ife mbeu, kuti tikhale ndi moyo, tisafe, ndi kuti
dziko lisakhale labwinja. 20Ndipo Yosefe anamgulira Farao dziko lonse la
Aigupto, cifukwa Aaigupto anagulitsa yense munda wace, cifukwa njala inakula
pa iwo; ndipo dziko linakhala la Farao. 21Tsono anthu, anasunthira iwo ku midzi

kucokera kumphepete kwa malire a Aigupto kufikira kumphepete kwina kwace. 22Koma dziko la ansembe lokha sanagule, cifukwa ansembe analandira gawo lao kwa Farao, nadya gawolo anawapatsa Farao; cifukwa cace sanagulitsa dziko lao. 23Ndipo Yosefe anati kwa anthu, Taonani, ndamgulira Farao inu ndi dziko lanu lero lomwe, taonani, mbeu zanu sizi, mubzale m'dziko. 24Ndipo padzakhala pakukunkha, muzipatsa limodzi la mwa magawo asanu kwa Farao, koma magawo anai ndi anu, mbeu za munda, ndi za cakudya canu, ndi ca ana anu ndi mabanja anu. 25Ndipo iwo anati, Watipulumutsa miyoyo yathu; tipeze ufulu pamaso pa mbuyanga, ndipo tidzakhala akapolo a Farao. 26Ndipo Yosefe analamulira lamulo la pa dziko la Aigupto kuukira lero, kuti Farao alandire limodzi la mwa magawo asanu; koma dziko la ansembe lokha silinakhala la Farao. 27Ndipo Israyeli anakhala m'dziko la Aigupto, m'dziko la Goseni; nakhala nazo zaozao m'menemo, nabalana nacuruka kwambiri.
28Ndipo Yakobo anakhala m'dziko la Aigupto zaka khumi mphambu zisanu ndi ziwiri; ndipo masiku a Yakobo zaka za moyo wace zinali zaka zana limodzi mphambu makumi anai kudza zisanu ndi ziwiri. 29Ndipo nthawi inayandikira kuti Israyeli adzafa, ndipo anaitana Yosefe mwana wace wamwamuna, nati kwa iye, Ngati ndapeza ufulu pamaso pako, ikatu dzanja lako pansi pa ncafu yanga, nundicitire ine zabwino ndi zoona: usandiikatu ine m'Aigupto; 30koma pamene ndidzagona ndi makolo anga, udzanditenge ine kuturuka m'dziko la Aigupto, ukandiike ine m'manda mwao. Ndipo iye anati, Ndidzacita monga mwanena. 31Ndipo anati, Undilumbirire ine; namlumbirira iye. Ndipo Israyeli anawerama kumutu kwa kama.

Genesis 48

Yakobo adalitsa ana a Yosefe

1Ndipo panali zitapita izi, anthu anati kwa Yosefe, Taonani, atate wanu
wadwala: ndipo iye anatenga ana ace amuna awiri, Manase ndi Efraimu, apite
naye. 2Ndipo anthu anamuuza Yakobo nati, Taonani, mwana wanu Yosefe
alinkudza kwa inu; ndipo Yakobo anadzilimbitsa, nakhala tsonga
pakama. 3Ndipo Yakobo anati kwa Yosefe, a Mulungu Wamphamvuyonse
anaonekera kwa ine pa Luzi m'dziko la Kanani nandidalitsa ine, nati kwa
ine, 4Taona, ndidzakubalitsa iwe, ndidzakucurukitsa iwe, ndidzakusandutsa iwe
khamu la anthu a mitundu; ndipo ndidzapatsa mbeu yako ya pambuyo pako
dziko ili likhale laolao cikhalire. 5Tsopano ana ako amuna awiri, amene
anakubadwira iwe m'dziko la Aigupto, ndisanadze kwa iwe ku Aigupto, ndiwo
anga; Efraimu ndi Manase, monga Rubeni ndi Simeoni, ndiwo anga. 6Koma
obala iwe udzawabala pambuyo pao, ndiwo ako; awaphe dzina la abale ao
m'colowa cao. 7Tsono ine, pamene ndinacokera ku Padani, Rakele anamwalira
pambali panga m'dziko la Kanani m'njira, itatsala nthawi yaing'ono tisadafike ku
Efrati; ndipo ndidamuika iye pamenepo pa njira ya ku Efrati (ndiwo
Betelehemu). 8Ndipo Israyeli anayang'ana ana amuna a Yosefe, nati, Ndani
awa? 9Ndipo Yosefe anati kwa atate wace, Amenewa ndi ana anga, amene
Mulungu wandipatsa ine pano. Ndipo iye anati, Udze naotu kwa ine, ndipo
ndidzawadalitsa. 10Koma maso a Israyeli anali akhungu m'ukalamba wace,
ndipo sanathei kuona. Ndipo anadza nao pafupi; ndipo anapsompsona iwo,
nawafungatira. 11Ndipo Israyeli anati kwa Yosefe, Sindinaganizira kuti ndione
nkhope yako: ndipo, taona, Mulungu wandionetsa ine mbeu zako
zomwe. 12Ndipo Yosefe anaturutsa iwo pakati pa maondo ace, nawerama ndi
nkhope yace pansi. 13Ndipo Yosefe anatenga iwo onse awiri, Efraimu m'dzanja
lace lamanja ku dzanja lamanzere la Yakobo, ndi Manase m'dzanja lace
lamanzere ku dzanja lamanja la Israyeli, nadza nao pafupi ndi iye. 14Ndipo
Israyeli anatambalitsa dzanja lace lamanja, naliika pa mutu wa Efraimu, amene
ndiye wamng'ono, ndi dzanja lace lamanzere pa mutu wa Manase
anapingasitsa manja ace dala; cifukwa Manase anali woyamba. 15Ndipo
anadalitsa Yosefe, nati, Mulungu, pamaso pace anayenda makolo anga
Abrahamu ndi Isake, Mulungu amene anandidyetsa ine nthawi zonse za moyo
wanga kufikira lero, 16mthenga amene anandiombola ine ku zoipa zonse,
adalitse anyamatawa; dzina langa lichulidwe pa iwo, ndi dzina la makolo anga
Abrahamu ndi Isake; iwo akule, nakhale khamu pakati pa dziko
lapansi. 17Ndipo pamene Yosefe anaona kuti atate wace anaika dzanja lace
lamanja pa mutu wa Efraimu, kudamuipira iye; ndipo anatukula dzanja la atate
wace, kulicotsa pa mutu wa Efraimu ndi kuliika pa muta wa Manase. 18Ndipo
Yosefe anati kwa atate wace, Msatero atate wanga, cifukwa uyu ndi woyamba;
ikani dzanja lanu lamanja pa mutu wace. 19Koma anakana atate wace, nati,
Ndidziwa mwananga, ndidziwa; Iyenso adzakhala mtundu wa anthu, iyenso
adzakula; koma mphwace adzakhala wamkuru ndi iye, ndipo mbeu zace
zidzakhala mitundu yambirimbiri. 20Ndipo anadalitsa iwo tsiku lomwelo, nati,
Mwa iwe Israyeli adzadalitsa, kuti, Mulungu akuyese iwe monga Efraimu ndi
monga Manase; ndipo anaika Efraimu woyamba wa Manase. 21Ndipo Israyeli
anati kwa Yosefe, Taona, ndirinkufa ine; Mulungu adzakhala ndi iwe,

adzakubwezanso iwe ku dziko la makolo ako. 22Ndipo ine ndakupatsa iwe gawo limodzi loposa la abale ako, limene ndinalanda m'dzanja la Aamori ndi lupanga langa ndi uta wanga.

Genesis 49

Yakobo adalitsa ana ace namwalira

1Ndipo Yakobo anaitana ana ace amuna, nati, Sonkhanani inu, kuti ndikuuzeni
inu cimene cidzakugwerani inu masiku akudzawo.
2Sonkhanani, tamvani, ana amuna a Yakobo:
Tamverani Israyeli atate wanu:
3Rubeni, ndiwe woyamba wanga, mphamvu yanga ndi ciyambi ca mphamvu
yanga;
Ulemu wopambana, ndi mphamvu yopambana.
4Wobwabwada ngati madzi; sudzapambana;
Cifukwa unakwera pa kama wa atate wako;
Pamenepo unaipitsapo; anakwera paja ndigonapo.
5Simeoni ndi Levi ndiwo abale;
Zida za mphulupulu ndizo malupanga ao.
6Mtima wangawe, usalowe mu ciungwe cao;
Ulemerero wanga, usadziphatike pa masonkhano ao;
Cifukwa m'kukwiya kwao anapha munthu,
M'kufuna kwao anapundula ng'ombe.
7Kutembereredwekukwiyakwao, cifukwa kunali koopsya;
Ndi kupsya mtima kwao, cifukwa kunali kwankharwe;
Ndidzawagawanitsa m'Yakobo
Ndidzabalalitsa iwo m'Israyeli.
8Yuda, abale ako adzakuyamika iwe;
Dzanja lako lidzakhala pa khosi la adani ako;
Ana amuna a atate wako adzakuweramira.
9Yuda ndi mwana wa mkango,
Kucokera kuzomotola, mwananga, wakwera;
Anawerama pansi, anabwatama ngati mkango,
Ndipo ngati mkango waukazi; ndani adzamukitsa iye?
10Ndodo yacifumu siidzacoka mwa Yuda,
Kapena wolamulira pakati pa mapazi ace,
Kufikira atadza Silo;
Ndipo anthu adzamvera iye.
11Adamanga mwana wa kavalo wace pampesa,
Ndi mwana wa buru wace pa mpesa wosankhika;
Natsuka malaya ace m'vinyo,
Ndi copfunda cace m'mwazi wa mphesa.
12Maso ace adzafiira ndi vinyo,
Ndipo mana ace adzayera ndi mkaka.
13Zebuloni adzakhala m'doko la kunyanja;
Ndipo iye adzakhala doko la ngalawa;
Ndipo malire ace adakhala pa Zidoni.
14Isakara ndiye buru wolimba,
Alinkugona pakati pa makola;
15Ndipo anaona popumulapo kuti panali pabwino,
Ndi dziko kuti linali lokondweretsa;
Ndipo anaweramitsa phewa lace kuti anyamule,

Nakhala kapolo wakugwira nchito ya msonkho,
16Dani adzaweruza anthu ace,
Monga limodzi la mafuko a Israyeli.
17Dani adzakhala njoka m'khwalala,
Songo panjira,
Imene iluma zitende za kavalo,
Kuti womkwera wace agwe cambuyo.
18Ndadikira cipulumutso canu, Yehova.
19Ndi Gadi, acifwamba adzampsinja iye;
Koma iye adzapsinja pa citende cao.
20Ndi Aseri, cakudya cace ndico mafuta,
Ndipo adzapereka zolongosoka zacifumu.
21Nafitali ndi nswala yomasuka;
Apatsa mau abwino.
22Yosefe ndi nthambi yobala,
Nthambi yobala pambali pa kasupe;
Nthambi zace ziyangayanga palinga.
23Eni uta anabvutitsa iye kwambiri,
Namponyera iye, namzunza:
24Koma uta wace unakhala wamphamvu,
Ndi mikono ya manja ace inalimbitsidwa
Ndi manja a Wamphamvu wa Yakobo.
(Kucokera kumeneko ndi mbusa, mwala wa Israyeli,)
25Ndi Mulungu wa atate wako amene adzakuthangata iwe,
Ndi Wamphamvuyonse, amene adzakudalitsa iwe
Ndi madalitso a Kumwamba,
Madalitso a madzi akuya akukhala pansi,
Madalitso a mabere, ndi a mimba.
26Madalitso a atate wako
Apambana mphamvu ndi madalitso a makolo anga,
Kufikira ku malekezero a patari a mapiri a cikhalire;
Adzakhala pa mutu wa Yosefe,
Ndi pakati pa mutu wa iye amene ali wolekanitsidwa ndi abale ace.
27Benjamini ndiye mmbulu wakulusalusa;
M'mamawa adzadya comotola,
Madzulo adzagawa zofunkha.
28Awa onse ndiwo mafuko khumi ndi awiri a Israyeli: izo ndizo zomwe ananena kwa iwo atate wao nawadalitsa; yense monga mdalitso wace anawadalitsa. 29Ndipo analangiza iwo nati kwa iwo, Ine nditi ndisonkhanizidwe kwa anthu a mtundu wanga; mundiike ine pamodzi ndi makolo anga m'phanga liri m'munda wa Efroni Mhiti, 30m'phanga liri m'munda wa Makipela, umene uli patsogolo pa Mamre, m'dziko la Kanani, limene Abrahamu analigula kwa Efroni Mhiti pamodzi ndi munda, likhale poikira pace: 31pamenepo anaika Abrahamu ndi Sara mkazi wace; pamenepo anaika Isake ndi Rebeka mkazi wace: pamenepo ndinaika Leya: 32munda ndi phanga liri m'menemo, zinagulidwa

kwa ana a Heti. 33Pamene Yakobo anatha kulangiza ana ace amuna, anafunya
mapazi ace pakama, natsirizika, nasonkhanizidwa kwa anthu a mtundu wace.

Genesis 50

Kumwalira kwa Yosefe

1Ndipo Yosefe anagwapa nkhope ya atate wace, namlirira iye nampsompsona
iye. 2Ndipo Yosefe anauza akapolo ace asing'anga kutiakonze atate wace: ndi
mankhwala osungira thupi: ndipo asing'anga anakonza Israyeli. 3Ndipo anatha
masiku ace makumi anai a iye; cifukwa comweco amatsiriza masiku akukonza
thupi; ndipo Aaigupto anamlira iye masiki makumi asanu ndi awiri.
4Atapita masiku akumlira iye Yosefe anati kwa mbumba ya Farao kuti, Ngatitu
ndapeza ufulu pamase panu, nenanitu m'makutu a Parae kuti, 5Atate wanga
anandilumbi ritsa ine, kuti, Taona, ndirinkufa m'manda m'mene ndadzikonzeran
ndekha m'dziko la Kanani, m'menemo udzandiika ine. Tsopano mundi loletu,
ndikwereko, ndipite, ndikaike atate wanga, nditatero ndidzabwe ranso. 6Ndipo
Farao anati, Pita kaike atate wako, monga iye anaku lumbiritsa iwe. 7Ndipo
Yosefe anapita kukaika atate wace; ndipo anakwera pamodzi ndi akapolo onse
a Farao, ndi akuru a pa mbumba yace, ndi akuru onse a m'dziko la
Aigupto, 8ndi mbumba yonse ya Yosefe ndi abale ace, ndi mbumba ya atate
wace: ang'ono ao okha, ndi nkhosa zao, ndi ng'ombe zao, anazisiya m'dziko la
Goseni. 9Ndipo anakwera pamodzi ndi iye magareta ndi apakavalo; ndipo
panali khamc lalikuru. 10Ndipo anafika pa dwale la Atadi, liri tsidya lija la
Yordano, pamenepo anamlira maliro a atate wace masiku asanu ndi
limodzi. 11Ndipo pamene anthu okhala m'dzikomo; Akanani, anaona maliro a
m'dwale la Atadi, anati, Awa ndi maliro akuru a Aaigupto: cifukwa cace dzina la
pamenepo linachedwa Abeli-mizraimu, pali tsidya lija la Yordano. 12Ndipo ana
ace amuna anamcitira iye monga anawalamulira iwo; 13cifukwa kuti ana ace
amuna anamnyamula iye kulowa naye m'dziko la Kanani, ndi kumuika iye
m'phanga la munda wa Makipela, limene Abrahamu analigula pamodzi ndi
munda, likhale poikira pace, kwa Efroni Mhiti, patsogolo pa Mamre.
14Ndipo ataika atate wace, Yosefe mabwera ku Aigupto, iye ndi abale ace, ndi
onse amene anakwera pamodzi naye kukaika atate wace. 15Ndipo pamene
abale ace a Yosefe anaona kuti atate wao anafa, anati, Kapena Yosefe adzatida
ife, ndipo adzatibwezera ife zoipa zonse tidamcitira iye. 16Ndipo anatumiza
mthenga kwa Yosefe kuti, Atate wathu asanafe analamulira, kuti, 17Muziti
cotero kwa Yosefe, Mukhululukiretu tsopano kulakwa kwa abale anu, ndi
kucimwa kwao, cifukwa kuti anakucitirani inu coipa; tsopano mutikhululukiretu
kulakwa kwa aka polo a Mulungu wa atate wanu. Ndipo Yosefe analira pamene
iwo ananena ndi iye. 18Ndiponso abale ace anamuka namgwadira pamaso
pace; nati, Taonani, ife ndife akapolo anu. 19Ndipo Yosefe anati kwa iwo,
Musaope; pakuti ndiri ine kodi m'malo a Mulungu? 20Koma inu,
munandipangira ine coipa; koma Mulungu anacipangira cabwino, kuti kucitike
monga lero, kupulumutsa amoyo anthu ambiri, 21Ndipo tsopano musaope; Ine
ndidzacereza inu, ndi ana anu ang'ono. Ndipo anawatonthoza iwo mitima yao,
nanena nao mokoma mtima.
22Ndipo Yosefe anakhala m'Aigupto, iye, ndi mbumba ya atate wace; ndipo
Yosefe anakhala ndi movo zaka zana limodzi ndi khumi. 23Ndipo Yosefe
anaona ana a Efraimu a mbadwo wacitatu; ananso a Makiri mwana
wamwamuna wa Manase anabadwa pa maondo a Yosefe. 24Yosefe ndipo
anati kwa abale ace, Ndirinkufa ine, koma Mulungu adzaonekera kwa inu,

adzakucotsani inu m'dziko muno kubwera kunka ku dziko limene analumbirira kwa Abrahamu ndi kwa Isake, ndi kwa Yakobo 25Ndipo Yosefe analumbiritsa ana a Israyeli kuti, Mulungu adzaonekera kwa inu ndithu, ndipo mudzakwera nao mafupa anga kucokera kuno. 26Ndipo anafa Yosefe, anali wa zaka zana limodzi ndi khumi; ndipo anakonza thupi lace ndi mankhwala osungira, ndipo ariamuika iye m'bokosi m'Aigupto.

Exodus

Eksodo 1

Masautso a ana a Israyeli m'Aigupto

1NDIPO maina a ana a Israyeli, amene analowa m'Aigupto ndi Yakobo ndi awa, analowa
munthu ndi banja lace: 2Rubeni, Simeoni, Levi ndi Yuda; 3Isakara, Zebuloni, ndi
Benjamini; 4Dani ndi Nafitali, Gadi ndi Aseri. 5Ndipo amoyo onse amene anaturuka
m'cuunomwace mwa Yakobo ndiwo makumi asanu ndi awiri; kama Yosefe anali
m'Aigupto. 6Ndipo anafa Yosefe, ndi abale ace onse, ndi mbadwo uwo wonse. 7Ana a
Israyeli ndipo anaswana, nabalana, nacuruka, nakhala nazo mphamvu zazikuru; ndipo
dziko linadzala nao.
8Pamenepo inalowa mfumu yatsopano m'ufumu wa Aigupto, imene siinadziwa
Yosefe. 9Ndipo ananena ndi anthu ace, Taonani, anthu, ndiwo ana a Israyeli, acuruka,
natiposa mphamvu. 10Tiyeni, tiwacenjerere angacuruke, ndi kuphatikizana ndi adani athu
ikafika nkhondo, ndi kulimbana nafe, ndi kucoka m'dzikomo. 11Potero anawaikira akuru a
misonkho kuti awasautse ndi akatunduno. Ndipo anammangira Farao midzi yosungiramo
cuma, ndiyo Pitomu ndi Ramese. 12Koma monga momwe anawasautsiramo, momwemo
anacuruka, momwemonso anafalikira. Ndipo anabvutika cifukwa ca ana a
Israyeli. 13Ndipo Aaigupto anawagwiritsa ana a Israyeli nchito yosautsa; 14nawawitsa
moyo wao ndi nchito yolimba, ya dothi ndi ya njerwa, ndi nchito zonse za pabwalo, nchito
zao zonse zimene anawagwiritsa nzosautsa.

Anamwino sam vera mfumu

15Ndipo mfumu ya Aigupto inanena ndi anamwino a Ahebri, dzina lace la wina ndiye
Sifra, dzina la mnzace ndiye Puwa; 16ninati, Pamene muciza akazi a Ahebri nimuwaone
pamipando; akakhala mwana wamwamuna, mumuphe; akakhala wamkazi, akhale ndi
moyo. 17Koma anamwino anaopa Mulungu, ndipo sanacita monga mfumu ya Aigupto
inawauza, koma analeka ana amuna akhale ndi moyo. 18Ndipo mfumu ya Aigupto
inaitana anamwino, ninena nao, Mwacita ici cifukwa ninji, ndi kuleka ana amunawo akhale
ndi moyo? 19Ndipo anamwino ananena ndi Farao, Popeza akazi a Ahebri safanana ndi
akazi a Aigupto; pakuti ali ndi mphamvu, naona ana asanalike anamwino. 20Potero
Mulungu anawacitira zabwino anamwino; ndipo anthuwo anacuruka, nakhala nazo
mphamvu zazikuru. 21Ndipo kunatero kuti, popeza anamwino anaopa Mulungu, iye
anawamangitsira mabanja. 22Ndipo Farao analamulira anthu ace onse, ndi kuti, Ana
amuna onse akabadwa aponyeni m'nyanja, koma ana akazi onse alekeni amovo.

Eksodo 2

Kubadwa kwa Mose

1Ndipo anamuka munthu wa banja la Levi, natenga mwana wamkazi wa Levi. 2Ndipo
anaima mkaziyo, naonamwanawamwamuna; m'mene anamuona kuti ali wokoma,
anambisa miyezi itatu. 3Koma pamene sanathe kumbisanso, anamtengera kabokosi
kagumbwa, napakapo nkhunga ndi phula; naikamo mwanayo, nakaika pakati pa
mabango m'mbali mwa nyanja. 4Ndipo mlongo wace anaima patali, adziwe comwe
adzamcitira. 5Ndipo mwana wamkazi wa Farao anatsikira kukasamba m'nyanja; ndipo
atsikana ace anayendayenda m'mbali mwa nyanja; ndipo iye anaona kabokosi pakati pa
mabango, natuma mdzakazi wace akatenge. 6Pamene anakabvundukula, anapenya
mwanayo; ndipo, taonani, khandalo lirikulira. Ndipo anamva naye cifundo, nati, Uyu ndiye
wa ana a Ahebri. 7Pamenepo mlongo wace ananena ndi mwana wamkazi wa Farao,
Ndipite ine kodi kukuitanirani woyamwitsa wa Ahebri, akuyamwitsireni mwanayo? 8Ndipo
mwana wamkazi wa Farao ananena naye, Pita. Napita namwaliyo, nakaitana amace wa
mwanayo. 9Ndipo mwana wamkazi wa Farao ananena naye, Pita naye mwana uyu, ndi
kundiyamwitsira iye, ndidzakupatsa mphotho yako. Ndipo mkaziyo anatenga mwanayo,
namyamwitsa, 10Ndipo atakula mwanayo, anapita naye kwa mwana wamkazi wa Farao,
ndipo iye anakhala mwana wace. Ndipo anamucha dzina lace Mose, nati, Cifukwa
ndinambvuula m'madzi.

11Ndipo kunali masiku amenewo, atakula Mose, kuti anaturukira kukazonda abale ace,
napenya akatundu ao; ndipo anaona munthu M-aigupto ali kukantha Mhebri, wa abale
ace. 12Ndipo anaunguza kwina ndi kwina, ndipo pamene anaona kuti palibe munthu,
anakantha M-aigupto, namfotsera mumcenga. 13M'mawa mwace anaturukanso, ndipo,
taonani, anthu awiri Ahebri alikugwirana; ndipo ananena ndi wocimwayo, kuti,
Umpandiranji mnzako? 14Koma anati, Wakuika iwe ndani ukhale mkuru ndi woweruza
wathu? kuteroku ukuti undiphe, monga unamupha M-aigupto? Ndipo Mose anacita
mantha, nanena, Ndithu cinthuci cadziwika. 15Pamene Farao anacimva ici, anafuna
kupha Mose. Koma Mose anathawa pankhope pa Farao, nakhala m'dziko la Midyani;
nakhala pansi pacitsime. 16Ndipo wansembe wa Midyani anali nao ana akazi asanu ndi
awiri, amene anadza kudzatunga madzi; ndipo anadzaza mimweco kuti amwetse gulu la
atate wao. 17Pamenepo anadza abusa nawapitikitsa; koma Mose anauka nawathandiza,
namwetsa gulu lao. 18M'mene anafika kwa Rehueli atate wao, iye anati, Mwabwera
msanga bwanji lero? 19Ndipo anati two, Munthu M-aigupto anatilanditsa m'manja a
abusa, natitungiranso madzi okwanira, namwetsa gululi. 20Ndipo anati kwa ana ace
akazi, Ali kuti iye? Mwamsiyiranji munthuyo? Kamuitaneni, adzadye cakudya. 21Ndipo
Mose anabvomera kukhala naye munthuyo; ndipo anampatsa Mose mwana wace
wamkazi Zipora. 22Ndipo anaona mwana, ndi Mose anamucha dzina lace Gerisomu;
pakuti anati, Ndakhala mlendo m'dziko la eni.

23Ndipo kunali pakupita masiku ambiri aja, idafa mfumu ya Aigupto; ndi ana a Israyeli
anatsitsa moyo cifukwa ca ukapolo wao, nalira, ndi kulira kwao kunakwera kwa
Mulungucifukwa ca ukapolowo. 24Ndipo Molungu anamva kubuula kwao, ndi Mulungu
anakumbukila cipangano cace ndi Abrahamu, ndi Isake, ndi Yakobo. 25Ndipo Molungu
anapenya Aisrayeli, ndi Mulungu anadziwa.

Eksodo 3

1Koma Mose analikuweta gulu la Yetero mpongozi wace, wansembe wa ku Midyani; natsogolera gululo m'tsogolo mwa cipululu, nafika ku phiri la Mulungu, ku Horebe. 2Ndipo mthenga wa Molungu anamuonekera m'cirangali camoto coturuka m'kati mwa citsamba; ndipo anapenya, ndipo taonani, citsamba cirikuyaka moto, koma cosanyeka citsambaco. 3Ndipo Mose anati, Ndipatuketu, ndikaone cooneka cacikuruco, citsambaco sicinyeka bwanji, 4Pamene Yehova anaona kuti adapatuka kukapenya, Mulungu ali m'kati mwa citsamba, anamuitana, nati, Mose, Mose. Ndipo anati, Ndiri pano. 5Ndipo iye anati, Usayandikire kuno; bvula nsapato zako ku mapazi ako, pakuti pamalo pamene upondapo iwe, mpopatulika. 6Ananenanso Ine ndine Mulungu wa atate wako, Molungu wa Abrahamu, Molungu wa Isake, ndi Mulungu wa Yakobo. Ndipo Mose anabisa nkhope yace; popeza anaopa kuyang'ana Mulungu, 7Ndipo Yehova anati, Ndapenyetsetsa mazunzo a anthu anga ali m'Aigupto, ndamvanso kulira kwao cifukwa ca akuwafulumiza; pakuti ndidziwa zowawitsa zao; 8ndipo ndatsikira kuwalanditsa m'manja a anthu a Aigupto, ndi kuwatumtsa m'dziko lila akwere nalowe m'dziko labwino ndi lalikuru, m'dziko moyenda mkaka ndi uci ngati madzi; ku malo a Akanani, ndi Ahiti ndi Aamori, ndi Aperizi, ndi Ahivi, ndi Ayebusi. 9Ndipo tsopano, taona kulira kwa ana a Israyeli kwandifikira; ndapenyanso kupsinjika kumene Aaigupto awapsinja nako. 10Tiye tsopano, ndikutuma kwa Farao, kuti uturutse anthu anga, ana a Israyeli m'Aigupto. 11Koma Mose anati kwa Mulungu, Ndine yani ine kuti ndipite kwa Farao, ndi kuti nditurutse ana a Israyeli m'Aigupto? 12Ndipo iye anati, Ine ndidzakhala ndi iwe; ndipo ici ndi cizindikilo ca iwe, cakuti ndakutuma ndine; utaturutsa anthuwo m'Aigupto mudzatumikira Mulungu paphiri pano. 13Ndipo Mose anati kwa Mulungu, Onani, pakufika ine kwa ana a Israyeli, ndi kunena nao, Mulungu wa makolo anu wandituma kwa inu; ndipo akakanena ndi ine, Dzina lace ndani? ndikanena nao ciani? 14Ndipo Molungu anati kwa Mose, INE NDINE YEMWE NDIRI INE. Anatinso, Ukatero ndi ana a Israyeli, INE NDINE wandituma kwa inu. 15Ndipo Mulungu ananenanso kwa Mose, Ukatero ndi ana a Israyeli, Yehova, Molungu wa makolo anu, Molungu wa Abrahamu, Mulungu wa Isake, ndi Molungu wa Yakobo anandituma kwa inu; ili nw dzina langa nthawi yosatha, ici ndi cikumbukiro canga m'mibadwo mibadwo. 16Muka, nukasonkhanitse akuru a Israyeli, nunene nao, Yehova, Mulungu wa makolo anu anandionekera ine, Mulungu wa Abrahamu, Isake ndi Yakobo, ndi kuti; Ndakuzondani ndithu, ndi kuona comwe akucitirani m'Aigupto; 17ndipo ndanena, Ndidzakukwezani kukuturutsani m'mazunzo a Aigupto, kukulowezani m'dziko la Akanani, ndi Ahiti, ndi Aamori, ndi Aperizi, ndi Ahivi, ndi Ayebusi, m'dziko moyenda mkaka ndi uci ngati madzi. 18Ndipo adzamveca mau ako; ndipo ukapite iwe ndi akuru a Israyeli, kwa mfumu ya Aigupto, ndi kukanena naye, Yehova, Mulungu wa Ahebri wakomana ndi ife; tiloleni, timuke tsopano ulendo wa masiku atatu m'cipululu, kuti timphere nsembe Yehova Mulungu wathu. 19Koma Ine ndidziwa kuti mfumu ya Aigupto siidzalola inu kumuka, inde lingakhale ndi dzanja lamphamvu ai. 20Ndipo ndidzatambasula dzanja langa, ndi kukantha Aigupto ndi zozizwa zanga zonse ndizicita pakati pace; ndi pambuyo pace adzakulolani kumuka. 21Ndipo ndidzapatsa anthu awa ufulu pamaso pa anthu a Aigupto; ndipo kudzakhala, pamene muturuka simudzaturuka opanda kanthu; 22koma mkazi yense adzafunse mnzace, ndi mlendo wokhala m'nyumba mwace, ampatse zokometsera zasiliva, ndi zokometsera zagolidi, ndi zobvala; ndipo mudzabveke nazo ana anu amuna ndi akazi; ndipo mudzafunkhe za Aaigupto.

Eksodo 4

Mose alandira mphamvu yakucita zodabwiza

1Ndipo Mose anayankha nati, Koma taonani, sadzakhulupirira ine, kapena kumvera mau
anga; pakuti adzanena, Yehova sanakuonekera iwe. 2Ndipo Yehova ananena naye, Ico
nciani m'dzanja lako? Nati, Ndodo. 3Ndipo ananena iye, Iponye pansi. Naiponya pansi,
ndipo inasanduka njoka; ndipo Mose anaithawa. 4Koma Yehova anati kwa Mose,
Tambasula dzanja lako, nuigwire kumcira; ndipo anatambasula dzanja lace, naigwira,
nikhalanso ndodo m'dzanja lace; 5kuti akhulupirire kuti wakuonekera Yehova Mulungu wa
makolo ao, Mulungu wa Abrahamu, Mulungu wa Isake, ndi Mulungu wa Yakobo. 6Ndipo
Yehova ananenanso naye, Longa dzanja lako pacifuwa pako. Ndipo analonga dzanja lace
pacifuwa pace, naliturutsa, taonani, dzanja lace linali lakhate, lotuwa ngati cipale
cofewa. 7Ndipo ananena iye, Bwerezanso dzanja lako pacifuwa pako. Ndipo
anabwerezanso dzanja lace pacifuwa pace; naliturutsa pacifuwa pace, taonani,
linasandukanso lomwe lakale. 8Ndipo kudzatero, ngati sakhulupirira iwe, ndi kusamvera
mau a cizindikilo coyamba, adzakhulupirira mau a cizindikilo cotsirizaci. 9Ndipo
kudzatero, aka panda kukhulupirira zingakhale zizindikilo izi, ndi kusamvera mau ako,
ukatunge madzi a kunyanja, ndi kuthira pamtunda; ndi madzi watunga ku nyanjayo
adzasanduka mwazi pamtunda. 10Ndipo Mose anati kwa Yehova, Mverani, Ambuye, ine
ndine munthu wosowa ponena, kapena dzulo, kapena kale, kapena cilankhulire Inu ndi
kapolo wanu, pakuti ndine wa m'kamwa molemera, ndi wa lilime lolemera. 11Koma
Yehova ananena naye, Anampangira munthu m'kamwa ndani? Kapena analenga munthu
wosalankhula ndani, kapena wogontha, kapena wamaso, kapena wakhungu? Si ndine
Yehova kodi? 12Ndipo tsopano muka, ndipo Ine ndidzakhala m'kamwa mwako, ndi
kukuphunzitsa comwe ukalankhule. 13Koma anati, Mverani, Ambuye, tumizani pa dzanja
la iye amene mudzamtuma. 14Pamenepo mkwiyo wa Yehova unamyakira Mose, ndipo
anati, Nanga Aroni Mlevi mbale wako sialipo kodi? Ndidziwa kuti kulankhula alankhula.
Ndipo, taona, aturuka kudzakomana ndiwe; ndipo pakuona iwe adzakondweram'mtima
mwace. 15Ndipo ukalankhule naye, ndi kumpangira mau; ndipo Ine ndidzakhala
m'kamwa mwako, ndi m'kamwa mwace, ndipo ndidzakuphunzitsani inu cimene
mukacite. 16Ndipo iye adzakulankhulira iwe kwa anthu; ndipo kudzatero, kuti iye
adzakhala kwa iwe ngati m'kamwa, ndi iwe udzakhala kwa iye ngati Mulungu. 17Ndipo
ukaigwire m'dzanja lako ndodo iyi, imene ukacite nayo zizindikilozo.

18Ndipo Mose anabwera namuka kwa Yetero mpongozi wace, nanena naye, Ndimuketu,
ndibwerere kumka kwa abale anga amene ali m'Aigupto, ndikaone ngati akali ndi moyo.
Ndipo Yetero ananena ndi Mose, Pita bwino. 19Ndipo Yehova ananena ndi Mose
m'Midyani, Muka, bwerera kumka ku Aigupto; pakuti adafa anthu onse amene anafuna
moyo wako. 20Pamenepo Mose anatenga mkazi wace ndi ana ace amuna, nawakweza
pa buru, nabwerera kumka ku dziko la Aigupto; ndipo Mose anagwira ndodo ya Mulungu
m'dzanja lace. 21Ndipo Yehova ananena ndi Mose, Pakumuka iwe kubwerera kumka ku
Aigupto, usamalire ucite zozizwa zonse ndaziika m'dzanja lako, pamaso pa Farao; koma
Ine ndidzalimbitsa mtima wace kuti asadzalole anthu kupita. 22Pamenepo ukanene ndi
Farao, Atero Yehova, Mwana wanga, mwana wanga woyamba ndiye Israyeli. 23Ndipo
ndanena ndi iwe, Mlole mwana wanga amuke, kuti anditumikire Ine; koma wakana
kumlola kuti asamuke; taona, Ine ndidzamupha mwana wako wamwamuna, mwana wako
woyamba. 24Ndipo kunali panjira, kucigono, Yehova anakomana naye, nafuna
kumupha. 25Koma Zipora anatenga mpeni wamwala, nadula khungu la mwana wace,
naliponya pa mapazi ace; nati, Pakuti iwe ndiwe mkwati wanga wamwazi. Ndipo iye
anamleka. 26Pamenepo anati mkaziyo, Mkwati wamwazi iwe, cifukwa ca mdulidwe.

Mose akomana ndi Aroni

27Ndipo Yehova ananena ndi Aroni, Muka kucipululu kukakomana ndi Mose. Ndipo
anamuka, nakomana naye pa phiri la Mulungu, nampsompsona. 28Ndipo Mose anauza
Aroni mau onse a Yehova amene adamtuma nao, ndi zizindikilo zonse zimene

adamlamulira. 29Pamenepo Mose ndi Aroni anamuka nasonkhanitsa akuru onse a ana a Israyeli; 30ndipo Aroni anawafotokozera mau onse amene Yehova adauza Mose, nacita zizindikilo zija pamaso pa anthu. 31Ndipo anthuwo anakhulupirira; ndipo pamene anamva kuti Yehova adawazonda ana a Israyeli, ndi kuti adaona mazunzo ao, anawerama, nalambira Mulungu.

Eksodo 5

Kupempha kwa Mose ndi Aroni kuipsa mlandu wa Aisrayeli

1Ndipo pambuyo pace Mose ndi Aroni analowa nanena ndi Farao, Atero
Yehova, Mulungu wa Israyeli, Lola anthu anga apite, kundicitira madyerero
m'cipululu. 2Koma Farao anati, Yehova ndani, kuti ndimvere mau ace ndi kulola
Israyeli apite? Sindimdziwa Yehova, ndiponso sindidzalola Israyeli apite. 3Ndipo
iwo anati, Mulungu wa Ahebri wakomana ndi ife; timuketu ulendo wa masiku
atatu m'cipululu, kumphera nsembe Yehova Mulungu wathu; kuti angatikumike
ndi mliri, kapena ndi lupanga, 4Ndipo mfumu ya Aigupto inanena nao, Inu,
Mose ndi Aroni, cifukwa ninji mumasulira anthu nchito zao? Mukani ku akatundu
anu. 5Farao anatinso, Taonani, anthu a m'dziko ndiwo ambiri tsopano; ndipo inu
muwapumitsa ku akatundu ao, 6Ndipo tsiku lomwelo Farao analamulira
akufulumiza anthu, ndi akapitao ao, ndi kuti, 7Musawapatsanso anthu udzu
wakupanga nao njerwa monga kale; apite okha adzifunire udzu. 8Ndipo
muziwawerengera njerwa, monga momwe anapanga kale; musacepsapo,
popeza acita cilezi; cifukwa cace alikupfuula, ndi kuti, Timuke, timphere nsembe
Mulungu wathu. 9Ilimbike nchito pa amunawo, kuti aigwiritsitse, asasamalire
mau amabodza. 10Ndipo akufulumiza anthu ndi akapitao ao anaturuka, nanena
ndi anthu ndi kuti, Atero Farao, Kulibe kukupatsani udzu. 11Mukani inu nokha,
dzifunireni udzu komwe muupeza; pakuti palibe kanthu kadzacepa pa nchito
yanu. 12Pamenepo anthuwo anabalalika m'dziko lonse la Aigupto kufuna ciputu
ngati udzu. 13Ndipo akufulumiza anawakakamiza, ndi kuti, Tsirizani nchito
zanu, nchito ya tsiku pa tsiku lace, monga muja munali ndi udzu. 14Ndipo
anapanda akapitao a ana a Israyeli, amene ofulumiza a Farao adawaika, ndi
kuti, Nanga dzulo ndi lero simunatsiriza bwanji nchito yanu yoneneka ya njerwa,
monga kale? 15Pamenepo akapitao a ana a Israyeli anafika nalirira Farao, nati,
Mwatero bwanji ndi akapolo anu? 16Udzu osawapatsa akapolo anu, ndipo
amanena ndi ife, Umbani njerwa; ndipo, taonani, amapanda akapolo anu; koma
kulakwa nkwa anthu anu. 17Koma iye anati, Aulesi inu, aulesi: cifukwa cace
mulikunena, Timuke, timphere nsembe Yehova. 18Mukani tsopano, gwirani
nchito; pakuti sadzakupatsani udzu, koma muonetse ciwerengero cace ca
njerwa. 19Ndipo akapitao a ana a Israyeli anaona kuti kudawaipira, pamene
ananena, Musamacepetsa njerwa zanu, nchito ya tsiku pa tsiku lace. 20Ndipo
poturuka kwa Farao iwo anakomana ndi Mose ndi Aroni, alikuima popenyana
nao; 21ndipo ananena nao, Yehova akupenyeni, naweruze; pakuti
mwatinyansitsa pamaso pa Farao, ndi pamaso pa anyamata ace, ndi
kuwapatsa lupanga m'dzanja lao kutipha nalo.

Mulungu alonjeza kupulumutso anthu ace

22Pamenepo Mose anabwerera namka kwa Yehova, nati, Ambuye,
mwawacitiranji coipa anthuwa? mwandituma bwanji? 23Popeza kuyambira kuja
ndinafika kwa Farao kulankhula m'dzina lanu, anawacitira coipa anthuwa; ndipo
simunalanditsa anthu anu konse.

1Ndipo Yehova ananena kwa Mose, Tsopano udzaona comwe ndidzacitira
Farao; pakuti ndi dzanja lamphamvu adzawalola apite, inde ndi dzanja
lamphamvu adzawaingitsa m'dziko lace.
2Ndipo Mulungu ananena ndi Mose, nati kwa iye, Ine ndine YEHOV A: 3ndipo
ndinaonekera Abrahamu, Isake ndi Yakobo, Mulungu Wamphamvuyonse; koma
sindinadziwika kwa iwo ndi dzina langa YEHOV A. 4Ndipo ndinakhazikitsanso
nao cipangano canga, kuwapatsa dziko la Kanani, dziko la maulendo ao, anali
alendo m'mwemo. 5Ndamvanso kubuula kwa ana a Israyeli, amene Aaigupto
awayesa akapolo; ndipo ndakumbukila cipangano canga. 6Cifukwa cace nena
kwa ana a Israyeli, Ine ndine Yehova, ndipo ndidzakuturutsani pansi pa
akatundu a Aaigupto, ndipo ndidzakulanditsani ku ukapolo wanu; ndipo
ndidzakuombolani ndi dzanja lotambasuka, ndi maweruzo akuru; 7ndipo
ndidzalandira inu mukhale anthu anga, ndipo ndidzakhala Ine Mulungu wanu;
ndipo mudzadziwa kuti Ine ndine Yehova Mulungu wanu, wakuturutsa inu pansi
pa akatundu a Aaigupto. 8Ndipo ndidzakulowetsani m'dziko limene ndinakweza
dzanja langa kunena za ilo, kuti ndilipereke kwa Abrahamu, kwa Isake ndi kwa
Yakobo; ndipo ndidzakupatsani ilo likhale lanulanu; Ine ndine Yehova. 9Ndipo
Mose ananena comweco ndi ana a Israyeli; koma sanamvera Mose cifukwa ca
kuwawa mtima, ndi ukapolo wolemera.
10Ndipo Yehova ananena ndi Mose, ndi kuti, 11Lowa, lankhula ndi Farao
mfumu ya Aigupto, kuti alole ana a Israyeli aturuke m'dziko lace. 12Koma Mose
ananena pamaso pa Mulungu, ndi kuti, Onani, ana a Israyeli sanandimvera ine;
adzandimvera bwanji Farao, ndine wa milomo yosadula? 13Ndipo Yehova
ananena ndi Mose ndi Aroni, nawalangiza za ana a Israyeli, ndi za Farao
mfumu ya Aigupto, kuti aturutse ana a Israyeli m'dziko la Aigupto.

Cibadwidwe ca Mose ndi Aroni

14Akuru a mbumba za makolo ao ndi awa: ana amuna a Rubeni, woyamba wa
Israyeli ndiwo: Hanoki ndi Palu, Hezroni, ndi Karmi; amene ndiwo mabanja a
Rubeni. 15Ndi ana amuna a Simeoni ndiwo: Yemweli, ndi Yamini, ndi Ohadi,
Yakini, ndi Zohari, ndi Sauli mwana wa mkazi wa m'Kanani; amene ndiwo
mabanja a Simeoni. 16Ndipo maina a ana amuna a Levi, mwa kubadwa kwao
ndiwo: Gerisoni, ndi Kohati, ndi Merari; ndipo zaka za moyo wa Levi ndizo zana
limodzi mphambu makumi atatu kudza zisanu ndi ziwiri. 17Ana amuna a
Gerisoni ndiwo: Libni ndi Simei, mwa mabanja ao. 18Ndi ana amuna a Kohati
ndiwo: Amramu ndi Izara, ndi Hebroni, ndi Uziyeli; ndipo zaka za moyo wa
Kohati ndizo zana limodzi ndi makumi atatu kudza zitatu. 19Ndipo ana amuna a
Merai ndiwo: Mali ndi Musi. Amenewo ndiwo mabanja a Levi mwa kubadwa
kwao. 20Ndipo Amramu anadzitengera Yokobedi mlongo wa atate wace akhale
mkazi wace; ndipo anambalira Aroni ndi Mose; ndi zaka za moyo wa Amramu
ndizo zaria limodzi mphambu makumi atatu kudza zisanu ndi ziwiri. 21Ndi ana
amuna a lzara ndiwo: Kora: ndi Nefegi, ndi Zikiri. 22Ndi ana amuna a Uziyeli
ndiwo: Misayeli, ndi Elisafana, ndi Sitiri. 23Ndipo Aroni anadzitengera Eliseba,
mwana wamkazi wa Aminadabu, mlongo wace wa Nasoni, akhale mkazi wace;
ndipo anambalira Nadabu ndi Abihu, Eleazara ndi ltamara. 24Ndipo ana amuna
a Kora ndiwo: Asiri ndi Elikana, ndi Abiasafu; amenewo ndiwo mabanja a
Akora. 25Ndipo Eleazara mwana wa Aroni anadzitengera mkazi wa ana akazi a

Putieli akhale mkazi wace, ndipo anambalira Pinehasi. Amenewo ndi akuru a
makolo a Alevi mwa mabanja ao. 26Omwewo ndiwo Aroni ndi Mose amene
Yehova ananena nao, Turutsani ana a Israyeli m'dziko la Aigupto mwa makamu
ao. 27Awa ndi omwewo ananena ndi Farao, mfumu ya Aigupto, awaturutse ana
a Israyeli m'Aigupto; Mose ndi Aroni amenewa.

Mulungu ampangira Mose

28Ndipo kunali, tsiku limene Yehova ananena ndi Mose m'dziko la
Aigupto, 29Yehova ananena ndi Mose, ndi kuti, Ine ndine Yehova: lankhula ndi
Farao mfumu ya Aigupto zonsezi Ine ndizinena nawe. 30Koma Mose anati
pamaso pa Yehova, Onani, ine ndiri wa milome yosadula, ndipo Farao
adzandimvera bwanji?

1Ndipo Yehova ananena ndi Mose, Taona, ndakuika ngati Mulungu kwa Farao;
ndi Aroni mkuru wako adzakhala mneneri wako. 2Iwe uzdankhula zonse
ndikulamulira; ndi Aroni mkuru wako azilankhula kwa Farao, kuti alole ana a
Israyeli aturuke m'dziko lace. 3Koma Ine ndidzaumitsa mtima wace wa Farao,
ndipo ndidzacurukitsa zizindikilo ndi zozizwa zanga m'dziko la Aigupto. 4Koma
Farao sadzamvera inu, ndipo ndidzaika dzanja langa pa Aigupto, ndipo
ndidzaturutsa makamu anga, anthu anga ana a Israyeli, m'dziko la Aigupto ndi
maweruzo akuru. 5Ndipo Aaigupto adzadziwa kuti Ine ndine Yehova,
pakutambasula Ine dzanja langa pa Aigupto, ndi kuturutsa ana a Israyeli pakati
pao. 6Ndipo Mose ndi Aroni anacita monga Yehova anawalamulira, momwemo
anacita. 7Ndipo Mose anali nazo zaka makumi asanu ndi atatu, ndi Aroni anali
nazo zaka makumi asanu ndi atatu kudza zitatu, pamene ananena ndi Farao.

Mose ndi amatsenga

8Ndipo Yehova ananena ndi Mose ndi Aroni, ndi kuti, 9Pamene Farao
adzalankhula nanu, ndi kuti, Dzicitireni codabwiza; pamenepo uzinena ndi
Aroni, Tenga ndodo yako, Iponye pansi pamaso pa Farao, isanduke
cinjoka, 10Ndipo Mose ndi Aroni analowa kwa Farao, nacita monga momwe
Yehova adawalamulira; ndipo Aroni anaponya pansi ndodo yace pamaso pa
Farao, ndi pamaso pa anyamata ace, ndipo inasanduka cinjoka, 11Pamenepo
Farao anaitananso anzeru, ndi amatsenga; ndipo alembi a Aigupto, iwonso
anacita momwemo ndi matsenga ao. 12Pakuti yense anaponya pansi ndodo
yace, ndipo zinasanduka zinjoka; koma ndodoya Aroni inameza ndodo
zao, 13Koma mtima wa Farao unalimba, ndipo sanamvera iwo; monga
adalankhula Yehova.

Cozizwitsa coyamba: Madzi asanduka mwazi

14Ndipo Yehova ananena ndi Mose, Walemera mtima wa Farao, akana kulola
anthu apite, 15Muka kwa Farao m'mawa; taona, aturuka kumka kumadzi;
nuime kumlinda m'mbali mwa nyanja; ndi ndodo idasanduka njokayo uigwire
m'dzanja lako. 16Ndipo ukanena naye, Yehova, Mulungu wa Ahebri anandituma
kwa inu, ndi kuti, Lola anthu anga amuke kuti anditumukire m'cipululu; koma,
taona, sunamvera ndi pano. 17Atero Yehova, Ndi ici udzadziwa kuti Ine ndine
Yehova: taonani, ndidzapanda madzi ali m'nyanja ndi ndodo iri m'dzanja langa,
ndipo adzasanduka mwazi. 18Ndi nsomba ziri m'nyanja zidzafa, ndi nyanja
idzanunkha; ndi Aaigupto adzacita mtima useru ndi kumwa madzi a
m'nyanjamo. 19Ndipo Yehova anati kwa Mose, Nena ndi Aroni, Tenga ndodo
yako, nutambasule dzanja lako pa madzi a m'Aigupto, pa nyanja yao, pa
ngalande zao, ndi pa matamanda ao, ndi pa matawale ao onse amadzi, kuti
asanduke mwazi; mukhale mwazi m'dziko lonse la Aigupto, m'zotengera
zamtengo, ndi zamwala. 20Ndipo Mose ndi Aroni anacita monga momwe
Yehova adawalamulira; nasamula ndodo, napanda madzi ali m'nyanjamo
pamaso pa Farao, ndi pamaso pa anyamata ace; ndipo madzi onse a
m'nyanjamo anasanduka mwazi. 21Ndi nsomba za m'nyanjamo zinafa; ndi
nyanjayo inanunkha; ndipo Aaigupto sanakhoza kumwa madzi a m'nyanjamo;
ndipo munali mwazi m'dziko lonse la Aigupto. 22Ndipo alembi a Aigupto anacita
momwemo ndi matsenga ao; koma mtima wa Farao unalimba, ndipo
sanamvera iwo; monga adalankhula Yehova. 23Ndipo Farao anatembenuka,

nalowa m'nyumba yace, osasamalira ici comwe mumtima mwace. 24Koma Aaigupto onse anakumba m'mphepete mwa nyanja kufuna madzi akumwa; pakuti sanakhoza kumwa madzi a m'nyanjamo. 25Ndipo anafikiramasiku asanu ndi awiri atapanda nyanja Yehova.

Eksodo 8

Cozizwitsa caciwiri: Acule

1Ndipo Yehova anati kwa Mose, Lowa kwa Farao, nunene naye, Atero Yehova, Lola anthu anga amuke, kuti anditumikire. 2Ndipo ukakana kuwalola amuke, taona, Ine ndidzapanda dziko lako lonse ndi acule; 3ndipo m'nyanjamo mudzacuruka acule, amene adzakwera nadzalowa m'nyumba mwako, ndi m'cipinda cogona iwe, ndi pakama pako, ndi m'nyumba ya anyamata ako, ndi pa anthu ako, m'micembo yanu yooceramo, ndi m'mbale zanu zoumbiramo. 4Ndipo acule adzakwera pa iwe, ndi pa anthu ako, ndi pa anyamata ako onse. 5Ndipo Yehova anati kwa Mose, Nena ndi Aroni, Tambasula dzanja lako ndi ndodo yako, panyanja, pangalande, ndi pamatamanda, nukweretse acule pa dziko la Aigupto. 6Ndipo Aroni anatambasula dzanja lace pa madzi a m'Aigupto; ndipo anakwera acule, nakuta dziko la Aigupto. 7Ndipo alembi anacita momwemo ndi matsenga ao, nakweretsa acule pa dziko la Aigupto. 8Pamenepo Farao anaitana Mose ndi Aroni, nati, Mundipembere Yehova, kuti andicotsere ine ndi anthu anga aculewo; ndipo ndidzalola anthu amuke, kuti amphere Yehova nsembe. 9Koma Mose anati kwa Farao, Ulemu ndi wanu, wa ine ai; ndipembere inu ndi anyamata anu ndi anthu anu liti, kuti aonongeke aculewo, acokere inu ndi nyumba zanu, atsale m'nyanja mokha? 10Ndipo anati, Mawa. Nati Mose, Kukhale monga mau anu, kuti mudziwe, kuti palibe wina wonga Yehova Mulungu wathu. 11Ndipo acule adzacokera inu, ndi nyumba zanu, ndi anyamata anu, ndi anthu anu; adzatsala m'nyanja mokha. 12Ndipo Mose ndi Aroni anaturuka kwa Farao; ndi Mose anapfuulira kwa Yehova kunena za acule amene adawaika pa Farao. 13Ndipo Yehova anacita monga mwa mau a Mose; nafa aculewo kucokera m'zinyumba, ndi m'mabwalo, ndi m'minda. 14Ndipo anawaola miulu-miulu; ndi dziko linanunkha. 15Koma pamene Farao, anaona kuti panali kupuma, anaumitsa mtima wace, osamvera iwo; monga adalankhula Yehova.

Cozizwitsa cacitatu: Nsabwe

16Ndipo Yehova anati kwa Mose, Nena ndi Aroni, Samula ndodo yako, nupande pfumbi lapansi, kuti lisanduke nsabwe m'dziko lonse la Aigupto. 17Ndipo anacita comweco; pakuti Aroni anasamula dzanja lace ndi ndodo yace, napanda pfumbi lapansi, ndipo panali nsabwe pa anthu ndi pa zoweta; pfumbi lonse lapansi liinasanduka nsabwe m'dziko lonse la Aigupto. 18Alembi anateronso ndi matsenga ao kuonetsa nsabwe, koma sanakhoza; ndipo panali nsabwe pa anthu, ndi pa zoweta. 19Pamenepo alembi anati kwa Farao, Cala ca Mulungu ici; koma mtima wa Farao unalimba, osamvera iwo; monga adalankhula Yehova.

Cozozwitsa cacinai: Mizaza

20Ndipo Yehova anati kwa Mose, Uuke ulawire mamawa, nuime pamaso pa Farao; taona, aturuka kumka kumadzi; nunene naye, Atero Yehova, Lola anthu anga amuke, anditumikire. 21Pakuti ukapanda kulola anthu anga amuke, taona, ndidzatuma mizaza pa iwe, ndi pa anyamata ako, ndi pa anthu ako, ndi pa nyumba zako; ndipo nyumba za Aaigupto zidzadzala nayo mizaza, ndi nthaka yomwe imene ikhalapo. 22Ndipo tsiku ilo ndidzalemba malire dziko la Goseni, m'mene mukhala anthu anga, kuti pamenepo pasakhale mizaza; kotero kuti

udziwe kuti Ine ndine Yehova pakati pa dzikoli. 23Ndipo ndidzaika cosiyanitsa pakati pa anthu anga ndi anthu ako; mawa padzakhala cizindikilo ici. 24Ndipo Yehovaanacita comweco; ndipo kunafika magulu a mizaza m'nyumba ya Farao, ndi m'nyumba za anyamata ace, ndi m'dziko lonse la Aigupto; dziko linaipatu cifukwa ca mizazayo. 25Pamenepo Farao anaitana Mose ndi Aroni, nati, Mukani, mphereni nsembe Mulungu wanu m'dzikomu. 26Koma Mose anati, Sikuyenera kutero; pakuti tidzamphera Yehova Mulungu wathu conyansa ca Aaigupto; taonani, ngati tikamphera nsembeconyansaca Aaigupto pamaso pao sadzatiponya miyala kodi? 27Timuke ulendo wa masiku atatu m'cipululu, tikamphere Yehova Mulungu wathu nsembe, monga adzanena nafe. 28Ndipo Farao anati, Ndidzakulolani mumuke, kuti mukamphere nsembe Yehova. Mulungu wanu m'cipululu; komatu musamuke kutaritu: mundipembere. 29Ndipo Mose anati, Onani, ndirikuturuka ine kwanu, ndidzapemba Yehova kuti mizaza icoke mawa kwa Farao, ndi kwa anyamata ace, ndi kwa anthu ace; komatu, Farao asanyengenso ndi kukana kulola anthuwa amuke kukamphera nsembe Yehova. 30Ndipo Mose anaturuka kwa Farao, napemba Yehova. 31Ndipo Yehova anacita monga mwa mau a Mose; nacotsera Farao ndi anyamata ace ndi anthu ace mizazayo, sunatsala ndi umodzi wonse. 32Koma Farao anaumitsa mtima wace nthawi yomweyonso, ndipo sanalola anthu amuke.

Eksodo 9

Cozizwitsa cacisanu: Kalira pa zoweta

1Pamenepo Yehova anati kwa Mose, Lowa kwa Farao, numuuze, Atero Yehova
Mulungu wa Ahebri, Lola anthu anga amuke, kuti anditumikire. 2Pakuti ukakana
kuwalola amuke, ndi kuwagwira cigwiritsire, 3taona, dzanja la Yehova
lidzakhala pa zoweta zako za kubusa, pa akavalo, pa aburu, pa ngamila, pa
ng'ombe, ndi pa zoweta zazing'ono ndi kalira woopsa. 4Ndipo Yehova
adzasiyanitsa pakati pa zoweta za Israyeli ndi zoweta za Aigupto; kuti kasafe
kanthu kali konse ka ana a Israyeli, 5Ndipo Yehova anaika nthawi yakuti, nati,
Mawa Yehova adzacita cinthu ice m'dzikomu. 6Ndipo m'mawa mwace Yehova
anacita cinthuco, ndipo zinafa zoweta zonse za m'Aigupto; koma sicinafa
cimodzi conse ca zoweta za ana a Israyeli. 7Ndipo Farao anatuma, taonani,
sicidafa cingakhale cimodzi comwe ca zoweta za Aisrayeli. Koma mtima wa
Farao unauma, ndipo sanalola anthu amuke.

Cozizwitsa ca 6: Zironda pa anthu ndi zoweta

8Ndipo Yehova ananena ndi Mose ndi Aroni, Tengani phulusa la ng'anjo lodzala
manja; ndi Mose aliwaze kuthambo pamaso pa Farao. 9Ndipo lidzakhala
pfumbi losalala pa dziko lonse la Aigupto, ndipo lidzakhala pa anthu ndi pa
zoweta ngati zironda zobuka ndi matuza, m'dziko lonse la Aigupto. 10Ndipo
anatenga phulusa la m'ng'anjo, naima pamaso pa Farao; ndi Mose analiwaza
kuthambo; ndipo linakhala zironda zobuka ndi matuza pa anthu ndi pa
zoweta. 11Ndipo alembi sanakhoza kuima pamaso pa Mose cifukwa ca
zirondaw; popeza panali zironda pa alembi ndi pa Aaigupto onse. 12Koma
Yehova analimbitsa mtima wa Farao, kuti sanamvera iwo; moga Yehova
adalankhula ndi Mose.

Cozizwitsa ca 7: Matalala

13Ndipo Yehova anati kwa Mose, Uka oulawire mamawa, nuime pamaso pa
Farao, nunene naye, Atero Yehova, Mulungu wa Ahebri, Lola anthu anga
amuke, akanditumikire. 14Pakuti nthawi yino ndidzatuma miliri yanga yonse
pamtima pako, ndi pa anayamata ako, ndi pa anthu ako; kuti udziwe kuti palibe
wina wonga Ine pa dziko lonse lapansi. 15Pakuti ndatambasula dzanja langa
tsopano, kuti ndikupande iwe ndi anthu ako ndi mliri, ndi kuti uonoogeke pa
dziko lapansi. 16Koma ndithu cifukwa cace ndakuimika kuti ndikuonetse
mphamvu yanga, ndi kuti alalikire dzina langa pa dziko lonse lapansi. 17Kodi
udzikwezanso pa anthu anga, ndi kusawalola amuke? 18Taona, mawa monga
nthawi yino ndidzabvumbitsa mbvumbi wa matalala, sipadakhala unzace
m'Aigupto kuyambira tsiku lija lidakhazikika kufikira lero lino. 19Ndipo tsopano,
tumiza, thawitsa zoweta zako ndi zonse uli nazo pabwalo; pakuti anthu onse ndi
zoweta zonse zopezeka pabwalo, zosasonkhanidwa m'nyumba, matalala
adzazigwera, ndipo zidzafa. 20Iyeyu wa anyamata a Farao wakuopa mau a
Yehova anathawitsira m'zinyumba anyamata ace ndi zoweta zace; 21koma
iyeyu wosasamalira mau a Yehova anasiya anyamata ndi zoweta zace
kubusa. 22Ndipo Yehova anati kwa Mose, Tambasula dzanja lako kuthambo,
kuti pakhale matalala pa dziko lonse la Aigupto, pa anthu ndi pa zoweta, ndi pa
zitsamba zonse za kuthengo, m'dziko la Aigupto. 23Pamenepo Mose
anasamulira ndodo yace kuthambo, ndipo Yehova anatumiza bingu ndi
matalala, ndi moto unatsikira pansi; ndipo Yehova anabvumbitsa matalala pa

dziko la Aigupto. 24Potero panali matalala, ndi mota wakutsikatsika pakati pa matalala, coopsa ndithu; panalibe cotere m'dziko lonse la Aigupto ciyambire mtundu wao. 25Ndipo matalala anapanda m'dziko lonse la Aigupto zonse za pabwalo, kuyambira anthu kufikira zoweta; ndipo matalala anapanda zitsamba zonse za kuthengo, nathyola mitengo yonse ya kuthengo. 26M'dziko la Goseni mokha, mokhala ana a Israyeli, munalibe matalala. 27Ndipo Farao anatumiza, naitana Mose ndi Aroni, nanena nao, Ndacimwa tsopano; Yehova ndiye wolungama, ine ndi anthu anga ndife oipa, 28Pembani kwa Yehova; cifukwa akwanira ndithu mabingu a Mulungu ndi matalala; ndipo ndidzakulolani mumuke, osakhalanso. 29Ndipo Mose ananena naye, Poturuka m'mudzi ine, ndidzasasatulira manja anga kwa Yehova; mabingu adzaleka, ndi matalala sadzakhalaponso; kuti mudziwe kuti dziko lapansi nla Yehova. 30Koma inu ndi anyamata anu ndidziwa kuti simudzayamba kuopa nkhope ya Yehova Mulungu. 31Ndipo thonje ndi barele zinayoyoka; pakuti barele lidafura, ndi thonje lidayamba maluwa. 32Koma tirigu ndi rai sizinayoyoka popeza amabzala m'mbuyo. 33Ndipo Mose anaturuka kwa Farao m'mudzi nasasatulira manja ace kwa Yehova; ndipo mabingu ndi matalala analeka, ndi mvula siinabvumbanso padziko. 34Pamene Farao anaona kuti mvula ndi matalala ndi mabingu zidaleka anaonjezanso kucimwa, naumitsa mtima wace, iye ndi anyamata ace. 35Potero mtima wa Farao unalimba, ndipo sanalola ana a Israyeli amuke; monga Yehova adalankhula mwa Mose.

Eksodo 10
Cozizwitsa ca 8: D'zombe
1Ndipo Yehova anati kwa Mose, Lowa kwa Farao; pakuti ndaumitsa mtima
wace, ndi mtima wa anyamata ace, kuti ndiike zizindikilo zanga izi pakati
pao; 2ndi kuti ufotokozere, m'makutu a ana ako, ndi a zidzukulu zako, comwe
ndidzacita m'Aigupto, ndi zizindikilo zanga zimene ndinaziika pakati pao; kuti
mudziwe kuti Ine ndine Yehova. 3Ndipo Mose ndi Aroni analowa kwa Farao
nanena naye, Atero Yehova, Mulungu wa Ahebri, Ukana kudzicepetsa pamaso
panga kufikira liti? Lola anthu anga amuke, akanditumikire; 4pakuti ukakana
kulola anthu anga amuke, taona, mawa ndidzafikitsa dzombe m'dziko
lako; 5ndipo lidzakuta nkhope ya dziko, kotero, kuti palibe munthu adzakhoza
kuona dziko; ndipo lidzadya zotsalira zidapulumuka, zidatsalira inu pamatalala,
ndipo lidzadya mtengo uti wonse wokuphukirani kuthengo; 6ndipo lidzadzaza
m'nyumba zako, ndi m'nyumba za anyamata ako onse, ndi m'nyumba za
Aaigupto onse; sanaciona cotere atate ako kapena makolo ako, kuyambira tsiku
lija lakukhala iwo pa dziko lapansi kufikira lero lino. Ndipo anatembenuka,
naturuka kwa Farao. 7Ndipo anyamata ace a Farao ananena naye, Ameneyo
amaticitira msampha kufikira liti? Lolani anthuwo amuke, akatumikire Yehova
Mulungu wao. Kodi simunayambe kudziwa kuti Aigupto laonongeka? 8Ndipo
anawabwereretsa Mose ndi Aroni kwa Farao, nanena nao, Mukani, katumikireni
Yehova Mulungu wanu. Koma amene adzapitawo ndiwo ani? 9Ndipo Mose
anati, Tidzamuka ndi ana athu ndi akuru athu, ndi ana athu amuna ndi akazi;
tidzamuka nazo nkhosa zathu ndi ng'ombe zathu; pakuti tiri nao madyerero a
Yehova. 10Ndipo ananena nao, Momwemo, Yehova akhale nanu ngati ndilola
inu ndi ana ang'ono anu mumuke; cenjerani, pakuti pali coipa pamaso
panu, 11Cotero ai, mukani tsopano, inu amuna akuru, tumikirani Yehova pakuti
ici mucifuna. Ndipo anawapitikitsa pamaso pa Farao.
12Ndipo Yehova anati kwa Mose, Tambasulira dzanja lako pa dziko la Aigupto,
lidze dzombe, kuti likwere pa dziko la Aigupto, lidye zitsamba zonse za m'dziko,
ndizo zonse adazisiya matalala. 13Pamenepo Mose analoza ndodo yace pa
dziko la Aigupto; ndipo Yehova anaombetsa padziko mphepo ya kum'mawa
usana wonse, ndi usiku womwe; ndipo kutaca mphepo ya kum'mawa inadza
nalo dzombe. 14Ndipo dzombe linakwera pa dziko lonse la Aigupto, ndipo
linatera pakati pa malire onse a Aigupto, lambirimbiri; lisanafike ili panalibe
dzombe lotere longa ili, ndipo litapita ili sipadzakhalanso lotere. 15Pakuti
linakuta nkhope ya dziko lonse kuti dziko linada; ndipo linadya zitsamba zonse
za m'dziko, ndi zipatso zonse za mitengo zimene matalala adazisiya; ndipo
sipanatsala cabiriwiri ciri conse, pamitengo kapena pa zitsamba za kuthengo,
m'dziko lonse la Aigupto. 16Pamenepo Farao anafulumira kuitana Mose ndi
Aroni; nati, Ndalakwira Yehova Mulungu wanu, ndi inu. 17Ndipo tsopano,
ndikhululukirenitu kulakwa kwanga nthawi yino yokha, nimundipembere kwa
Yehova Mulungu wanu, kuti andicotsere imfa yino yokha. 18Ndipo anaturuka
kwa Farao, napemba Yehova. 19Ndipo Yehova anabweza mphepo yolimbatu ya
kumadzulo, imene inapita nalo dzombe niliponya m'Nyanja Yofiira: silinatsala
dzombe limodzi pakati pa malire onse a Aigupto. 20Koma Yehova analimbitsa
mtima wa Farao, ndipo sanalola ana a Israyeli amuke.
Cozizwitsa ca 9: Mdima

21Ndipo Yehova anati kwa Mose, Tambasulira dzanja lako kuthambo, ndipo padzakhala mdima pa dziko la Aigupto, ndiwo mdima wokhudzika. 22Ndipo Mose anatambasulira dzanja lace kuthambo; ndipo munali mdima bii m'dziko lonse la Aigupto masiku atatu; 23sanaonana, sanaukanso munthu pamalo pace, masiku atatu; koma kwa ana onse a Israyeli kudayera m'nyumba zao. 24Ndipo Farao anaitana Mose, nati, Mukani, tumikirani Yehova; nkhosa zanu ndi ng'ombe zanu zokha zitsale; mumuke nao ana anu ang'ononso. 25Koma Mose anati, Mutipatsenso m'dzanja mwathu nsembe zophera ndi nsembe zopsereza, kuti timkonzere Yehova Mulungu wathu. 26Zoweta zathu zomwe tidzapita nazo; cosatsala ciboda cimodzi; pakuti mwa izo tiyenera kutenga zakutumikira nazo Yehova Mulungu wathu; ndipo tisanafikeko, sitidziwa umo tidzamtumikira Yehova. 27Koma Yehova analimbitsa mtima wace wa Farao, ndipo anakana kuwaleka amuke. 28Ndipo Farao ananena naye, Coka pano, uzicenjera usaonenso nkhope yanga; pakuti tsiku limene uonanso nkhope yanga udzafa. 29Ndipo Mose anati, Mwanena bwino; sindidzaonanso nkhope yanu.

Eksodo 11

Cozizwitsa cakhumi: Imfa ya ana oyamba kubadwa

1Ndipo Yehova ananena ndi Mose, Watsala moo umodzi ndidzamtengera
Farao, ndi Aigupto; pambuyo pace adzakulolani mucoke kuno; pamene
akulolani kupita, zoonadi adzakuingitsani kuno konse. 2Lankhula tsopano
m'makutu a anthu, kuti mwamuna yense apemphe kwa mnzace, ndi mkazi
yense kwa mnzace, zokometsera zasiliva ndi zagolidi. 3Ndipo Yehova
anawapatsa anthu cisomo pamaso pa Aaigupto. Munthuyo Mose ndiyenso
wamkuru ndithu m'dziko la Aigupto, pamaso pa anyamata a Farao, ndi pamaso
pa anthu.
4Ndipo Mose anati, Atero Yehova, Monga pakati pa usiku ndidzaturuka loe
kumka pakati pa Aigupto; 5ndipo ana onse oyamba a m'dziko la Aigupto adzafa,
kuyambira mwana woyamba wa Farao wokhala pa mpando wacifumu wace,
kufikira mwana woyamba wa mdzakazi wokhala pa miyala yopera; ndi ana onse
oyamba a zoweta. 6Ndipo kudzakhala kulira kwakukuru m'dziko lonse la
Aigupto, kunalibe kunzace kotere, sikudzakhalanso kunzace kotere. 7Koma
palibe garu adzafunyitsira lilime lace ana onse a Israyeli ngakhale anthu kapena
zoweta; kuti mudziwe kuti Yehova asiyanitsa pakati pa Aaigupto ndi
Aisrayeli. 8Ndipo anyamata ako onse awa adzanditsikira, nadzandigwadira, ndi
kuti, Turukani inu, ndi anthu onse akukutsatani; ndipo pambuyo pace
ndidzaturuka. Ndipo anaturuka kwa Farao wakupsa mtima.
9Ndipo Yehova anati kwa Mose, Farao sadzamvera inu; kuti zozizwa zanga
zicuruke m'dziko la Aigupto. 10Ndipo Mose ndi Aroni anacita zozizwa izi zonse
pamaso pa Farao; koma Yehova analimbitsa mtima wace wa Farao, ndipo
sanalola ana a Israyeli aturuke m'dziko lace.

Eksodo 12
Kuikidwa kwa Paskha
1Ndipo Yehova ananena ndi Mose ndi Aroni m'dziko la Aigupto, ndi kuti, 2Mwezi
uno uzikhala kwa inu woyamba wa miyezi; muziuyesa mwezi woyamba wa
caka. 3Mulankhule ndi msonkhano wonse wa Israyeli ndi kuti, Tsiku lakhumi la
mwezi uno adzitengere munthu yense mwana wa nkhosa, monga mwa
mabanja a atate ao, mwana wa nkhosa pabanja. 4Banja likaperewera mwana
wa nkhosa, munthu ndi mnzace ali pafupi pa nyumba yace atenge monga mwa
kufikira kwa anthu ao; muziwerengera mwana wa nkhosa monga mwa kudya
kwao. 5Mwana wa nkhosa wanu azikhala wangwiro, wamwamuna, wa caka
cimodzi; muzimtenga ku nkhosa kapena ku mbuzi. 6Ndipo mukhale naye
cisungire kufikira tsiku lakhumi ndi cinai la mwezi womwe; ndipo bungwe lonse
la anthu a Israyeli lizimupha madzulo. 7Ndipo azitengako mwazi, naupake pa
mphuthu za mbali ndi ya pamwamba m'nyumba zimene adyeramo. 8Ndipo
azidya nyamayo usiku womwewo, yooca pamoto, ndi mkate wopanda cotupitsa;
aidye ndi ndiwo zowawa, 9Musaidya yaiwisi, kapena yophika ndi madzi konse
ai, koma yooca pamoto; muti wace ndi miyendo yace ndi matumbo
ace. 10Ndipo musasiyako kufikira m'mawa; koma yotsalira kufikira m'mawayo
muipsereze ndi moto: 11Ndipo muziidya cotero: okwinda m'cuuno, nsapato
zanu pa mapazi anu ndodo yanu m'dzanja lanu, ndipo muziidya msanga; ndiye
Paskha wa Yehova. 12Pakuti ndidzapita pakati pa dziko la Aigupto usiku
womwewo, ndi kukantha ana oyamba onse m'dziko la Aigupto, anthu ndi
zoweta; ndipo ndidzacita maweruzo pa milungu yonse ya Aigupto; Ine ndine
Yehova. 13Ndipo mwaziwo udzakhala cizindikilo kwa inu pa nyumba zimene
mukhalamo; pamene ndiona mwaziwo ndidzapitirira inu, ndipo sipadzakhala
mliri wakukuonongani, pakukantha Ine dziko la Aigupto, 14Ndipo tsiku lino
lidzakhala kwa inu cikumbutso, muzilisunga la madyerero a Yehova; ku
mibadwo yanu muzilisunga la madyerero, likhale lemba losatha. 15Masiku
asanu ndi awiri muzidya mkate wopanda cotupitsa; lingakhale tsiku loyamba
muzicotsa cotupitsa m'nyumba zanu; pakuti ali yense wakudya mkate wa
cotupitsa kuyambira tsiku loyamba kufikira tsiku lacisanu ndi ciwiri, munthu
amene adzasadzidwa kwa Israyeli. 16Ndipo tsiku loyamba kukhale kusonkhana
kopatulika, ndi tsiku lacisanu ndi ciwiri kukhalenso kusonkhana kopatulika;
pasacitike nchito masikuwo, zokhazi zakudya anthu onse ndizo
muzicita. 17Ndipo muzisunga madyerero a mkate wopanda cotupitsa; pakuti
tsiku lomwe lino ndinaturutsa makamu anu m'dziko la Aigupto; cifukwa cace
muzisunga tsiku lino m'mibadwo yanu, lemba losatha. 18Mwezi woyamba, tsiku
lace lakhumi ndi cinai madzulo ace, muzidya mkate wopanda cotupitsa, kufikira
tsiku la makumi awiri mphambu limodzi la mwezi, madzulo ace. 19Cisapezeke
cotupitsa m'nyumba zanu masiku asanu ndi awiri; pakuti ali yense wakudya
kanthu ka cotupitsa, munthuyo adzasadzidwa ku msonkhano wa Israyeli,
angakhale ndiye mlendo kapena wobadwa m'dziko. 20Musadye kanthu ka
cotupitsa; mokhala inu monse muzidya mkate wopandacotupitsa.
21Pamenepo Mose anaitana akuru onse a Israyeli, nanena nao, Pitani,
dzitengereni ana a nkhosa monga mwa mabanja anu, nimuphere
Paskha. 22Ndipo muzitenga mpukutu wa hisope, ndi kuubviika m'mwazi uli
m'mbale, ndi kupaka mwazi uli m'mbalemo pa mphuthu ya pamwamba ndi

pambali; koma inu, asaturuke munthu pakhomo pa nyumba yace kufikira m'mawa. 23Pakuti Yehova adzapita pakatipo kukantha Aaigupto; koma pamene adzaona mwaziwo pa mphuthu pamwamba ndi za pambali, Yehova adzapitirira pakhomopo, osalola woonongaalowe m'nyumba zanu kukukanthani. 24Ndipo muzisunga cinthu ici cikhale lemba la kwa inu, ndi kwa ana anu ku nthawi zonse. 25Ndipo kudzakhala, pamene mulowa m'dziko limene Yehova adzakupatsani, mensa analankhula, muzisunga kutumikira kumeneku. 26Ndipo kudzakhala, pamene ana anu adzanena ndi inu, Kutumikiraku muli nako nkutani? 27mudzati, Ndiko nsembe ya Paskha wa Yehova, amene anapitirira nyumba za ana a Israyeli m'Aigupto, pamene anakantha Aaigupto, napulumutsa nyumba zathu. 28Ndipo anthu anawerama, nalambira. Ndipo ana a Israyeli anamuka nacita monga Yehova adalamulira Mose ndi Aroni; anacita momwemo.

Ana oyamba kubadwa aphedwa

29Ndipo panakhala pakati pa usiku, Yehova anakantha ana oyamba onse a m'dziko la Aigupto, kuyambira mwana woyamba wa Earao wakukhala pa mpando wacifumu wace kufikira mwana woyamba wa wam'nsinga ali m'kaidi; adi ana oyamba onse a zoweta. 30Ndipo Farao anauka usiku, iyendi anyamata ace onse, ndi Aaigupto onse; ndipo kunali kulira kwakukulu m'Aigupto; pakuti panalibe nyumba yopanda wakufa m'mwemo. 31Ndipo anaitana Mose ndi Aroni usiku, nati, Ukani, turukani pakati pa anthu anga, inu ndi ana a Israyeli; ndipo mukani katumikireni Yehova, monga mwanena. 32Muka nazoni zoweta zanu zazing'ono ndi zazikuru, monga mwanena; cokani, ndi kundidalitsa Inenso. 33Ndipo Aaigupto anaumiriza anthuwo, nafulumira kuwaturutsa m'dziko; pakuti anati, Tiri akufa tonse. 34Ndipo anthu anatenga mtanda wao usanatupe, ndi zoumbiramo zao zomangidwa m'zobvala zao pa mapewa ao. 35Ndipo ana a Israyeli anacita monga mwa mau a Mose; napempha Aaigupto zokometsera zasiliva, ndi zagolidi, ndi zobvala. 36Ndipo Yehova anapatsa anthu cisomo pamaso pa Aaigupto, ndipo sanawakaniza. Ndipo anawafunkhira Aaigupto.

Ana a Israyeli aturuka m'Aigupto

37Ndipo ana a Israyeli anayenda ulendo wakucokera ku Ramese kufikira ku Sukoti, zikwi mazana asanu ndi limodzi oyenda okha, ndiwo amuna, osawerenga ana. 38Ndipo anthu ambiri osokonezeka anakwera nao; ndi nkhosa ndi ng'ombe, zoweta zambirimbiri. 39Ndipo anaoca timitanda topanda cotupitsa ta mtanda umene anabwera nao ku Aigupto, popeza sadaikamo cotupitsa; pakuti adawapitikitsa ku Aigupto, ndipo sanathe kucedwa, kapena kudzikonzeratu kamba. 40Ndipo kukhala kwa ana a Israyeli anakhala m'Aigupto ndiko zaka mazana anai kudza makumi atatu. 41Ndipo kunakhala pakutha zaka mazana anai kudza makumi atatu, inde panakhala tsiku lomwelo, makamu onse a Yehova anaturuka m'dziko la Aigupto. 42Ndiwo usiku wosungira Yehova ndithu, cifukwa ca kuwaturutsa m'dziko la Aigupto; usiku womwe uno ukhale wosungira Yehova ana onse a Israyeli ku mibadwo yao.

Lamulo la Paskha

43Ndipo Yehova anati kwa Mose ndi Aroni, Lemba la Paskha ndi ili: mwana wa mlendo ali yense asadyeko; 44koma kapolo wa mwini ali yense, wogula ndi ndarama, utamdula, ndipo adyeko. 45Mlendo kapena wolembedwa nchito

asadyeko. 46Audye m'nyumba imodzi; usaturukira nayo kubwalo nyama yina; ndipo musathyole pfupa lace. 47Msonkhano wonse wa Israyeli uzicita ici. 48Koma akakhala nanu mlendo, nakonzera Yehova Paskha, adulidwe amuna ace onse, ndipo pamenepo asendere kuucita; nakhale ngati wobadwa m'dziko; koma wosadulidwa ali yense asadyeko. 49Pakhale lamulo lomweli pa wobadwa m'dziko, ndi pa mlendo wakukhala pakati pa inu. 50Ndipo ana onse a Israyeli anacita monga Yehova adawalamulira Mose ndi Aroni, momwemo anacita. 51Ndipo kunakhala tsiku lomwelo, kuti Yehova anaturutsa ana a Israyeli m'dziko la Aigupto, monga mwa makamu ao.

Eksodo 13

Ana ovamba kubadwa apatulidwira Yehova

1Ndipo Yehova ananena ndi Mose ndi kuti, 2Ndipatulire Ine yense woyamba
kubadwa, wotsegulira pa amace mwa ana a Israyeli, mwa anthu ndi mwa
zoweta; ndiwo anga.
3Ndipo Mose ananena ndi anthu, Kumbukirani tsiku linu limene munaturuka
m'Aigupto, m'nyumba ya akapolo; pakuti Yehova anakuturutsani muno ndi
dzanja lamphamvu; ndipo asadye kanthu ka cotupitsa. 4Muturuka lero lino
mwezi wa Abibu. 5Ndipo kudzakhala atakulowetsa Yehova m'dziko la Akanani,
ndi la Ahiti, ndi la Aamori ndi la Ahivi, ndi la Ayebusi, limene analumbira ndi
makolo ako kukupatsa, m'dziko moyenda mkaka ndi uci ngati madzi,
uzikasunga kutumikira kumeneku mwezi uno. 6Masiku asanu ndi awiri uzikadya
mkate wopanda cotupitsa, ndipo tsiku lacisanu ndi ciwiri likhale la madyerero a
Yehova. 7Azikadya mkate wopanda cotupitsa masiku asanu ndi awiriwo ndipo
kasaoneke kanthu ka cotupitsa kwanu; inde cotupitsa cisaoneke kwanu
m'malire ako onse. 8Ndipo ukauze mwana wako wamwamuna tsikulo, ndi kuti,
Nditero cifukwa comwe Yehova anandicitira ine poturuka ine m'Aigupto, 9Ndipo
cizikhala ndi iwe ngati cizindikilo pa dzanja lako, ndi cikumbutso pakati pa maso
ako; kuti cilamulo ca Yehova cikhale m'kamwa mwako; pakuti Yehova
anakuturutsa m'Aigupto ndi dzanja lamphamvu. 10Cifukwa cace uzikasunga
lemba ili pa nyengo yace caka ndi caka.
11Ndipo kudzakhala, atakulowetsa Yehova m'dziko la Akanani, monga
anakulumbirira iwe ndi makolo ako, ndipo anakupatsa ilo, 12kuti uzikapatulira
Yehova onse oyamba kubadwa ndi oyamba onse uli nao odzera kwa zoweta;
amunawo ndi a Yehova. 13Koma woyamba yense wa buru uzimuombola ndi
mwana wa nkhosa; ndipo ukapanda kumuombola uzimthyola khosi; koma
oyamba onse a munthu mwa ana ako uziwaombola. 14Ndipo kudzakhala,
akakufunsa mwana wako masiku akudzawo ndi kuti, Ici nciani? ukanene naye,
Yehova anatiturutsa m'Aigupto, m'nyumba ya aka polo, ndi dzanja
lamphamvu; 15ndipo kunakhala, pamene Farao anadziumitsa kuti tisamuke,
Yehova anawapha onse oyamba kubadwa m'dziko la Aigupto, kuyambira
oyamba a anthu, kufikira oyamba a zoweta; cifukwa cace ndimphera nsembe
Yehova zazimuna zoyamba kubadwa zonse; koma oyamba onse a ana anga
ndiwaombola. 16Ndipo cizikhala ngati cizindikilo pa dzanja lako, ndi
capamphumi pakati pa maso ako; pakuti Yehova anatiturutsa m'Aigupto ndi
dzanja lamphamvu.

Ulendo womka ku Nyanja Yofiira

17Ndipo kunakhala pamene Farao adalola anthu amuke, Mulungu
sanawatsogolera njira ya dziko la Afilisti, ndiyo yaifupi; pakuti Mulungu anati.
Angadodome anthuwo pakuona nkhondo ndi kubwerera m'mbuyo kumka ku
Aigupto. 18Koma Mulungu anawazungulitsa anthuwo, ku njira ya kucipululu ya
Nyanja Yofiira; ndipo ana a Israyeli anakwera kucokera m'dziko la Aigupto
okonzeka. 19Ndipo Mose anamuka nao mafupa a Yosefe; pakuti
adawalumbiritsatu ana a Israyeli ndi kuti, Mulungu adzakuzondani ndithu ndipo
mukakwere nao mafupa anga osawwya kuno. 20Ndipo anacokera ku Sukoti,
nagona ku Etamu, pa malekezero a cipululu. 21Ndipo Yehova anawatsogolera
usana ndi mtambo njo kuwatsogolera m'njira; ndi usiku ndi moto njo,

wakuwawalitsira; kuti ayende usana ndi usiku; 22sanacotsa mtambo usana, kapena mtambo wamoto usiku, pamaso pa anthu.

Eksodo 14

Farao alondola Aisrayeli

1Ndipo Yehova ananena ndi Mose, ndi kuti, 2Lankhula ndi anthu a Israyeli kuti abwerere m'mbuyo nagone patsogolo pa Pihahiroti, pakati pa Migidoli ndi nyanja yamcere, patsogolo pa Baala-Zefoni; pandunji pace mugone panyanja. 3Ndipo Farao adzanena za ana a Israyeli, Azimidwa dziko, cipululu cawatsekera. 4Ndipo ndidzalimbitsa mtima wace wa Farao kuti awalondole; ndipo ndidzalemekezedwa pa Farao ndi pa nkhondo yace yonse; pamenepo Aaigupto adzadziwa kuti Ine ndine Yehova, Ndipo anacita comweco. 5Ndipo anauza mfumu ya Aigupto kuti anthu adathawa; ndi mtima wa Farao ndi wa anyamata ace inasandulikira anthuwo, ndipo anati, Ici nciani tacita, kuti talola Israyeli amuke osatigwiriranso nchito? 6Ndipo anamanga gareta lace, napita nao anthu ace; 7napita nao magareta osankhika mazana asanu ndi limodzi, ndi magareta onse a m'Aigupto, ndi akapitao ao onse. 8Ndipo Yehova analimbitsa mtima wa Farao, mfumu ya Aigupto, ndipo iye analondola ana a Israyeli; koma ana a Israyeli adaturuka ndi dzanja lokwezeka. 9Ndipo Aaigupto anawalondola, ndiwo akavalo ndi magareta onse a Farao, ndi apakavalo ace, ndi nkhondo yace, nawapeza ali kucigono kunyanja, pa Pihahiroti, patsogolo pa Baala-Zefoni. 10Ndipo pamene Farao anayandikira ana a Israyeli anatukula maso ao, taonani, Aaigupto alinkutsata pambuyo pao; ndipo anaopa kwambiri; ndi ana a Israyeli anapfuulira kwa Yehova. 11Ndipo anati kwa Mose, Kodi mwaticotsera kuti tikafe m'cipululu cifukwa panahbe manda m'Aigupto? Nciani ici mwaticitira kuti mwatiturutsa m'Aigupto? 12Si awa maowo tinalankhula nanu m'Aigupto ndi kuti, Tliekeni, kuti tigwirire nchito Aaigupto? pakuti kutumikira Aaigupto kutikomera si kufa m'cipululu ai. 13Ndipo Mose ananena ndi anthu, Musaope, cirimikani, ndipo penyani cipulumutso ca Yehova, cimene adzakucitirani lero; pakuti Aaigupto mwawaona lerowa simudzawaonansokonse. 14Yehova adzakugwirirani nkhondo, ndipo inu mudzakhala cere.

Aisrayeli aoloka pouma

15Ndipo Yehova anati kwa Mose, Upfuuliranji kwa Ine? lankhula ndi ana a Israyeli kuti aziyenda. 16Ndipo iwe nyamula ndodo yako, nutambasulire dzanja lako kunyanja, nuigawe, kuti ana a Israyeli alowe pakati pa nyanja pouma. 17Ndipo Ine, taonani, ndilimbitsa mitima ya Aaigupto, kuti alowemo powatsata; ndipo ndidzalemekezedwa pa Farao, ndi pa nkhondo yace yonse, pa magareta ace, ndi pa okwera pa akavalo ace. 18Ndipo Aaigupto adzadziwa kuti Ine ndine Yehova, polemekezedwa Ine pa Farao, pa magareta ace, ndi pa okwera pa akavalo ace. 19Ndipo mthenga wa Mulungu, wakutsogolera ulendo wa Israyeli, unacokako, nutsata pambuyo pao; ndipo mtambo njo uja unacoka patsogolo pao, nuima pambuyo pao; 20nulowa pakati pa ulendo wa Aaigupto ndi ulendo wa Aisrayeli ndipo mtambo unacita mdima, komanso unaunikira usiku; ndipo ulendo wina sunayandikizana ndi unzace usiku wonse. 21Ndipo Mose anatambasulira dzanja lace kunyanja; ndipo Yehova anabweza nyanja ndi mphepo yolimba ya kum'mawa usiku wonse, naumitsa nyanja; ndipo madziwo anagawikana. 22Ndipo ana a Israyeli analowa pakati pa nyanja pouma; ndi madziwo anakhala kwa iwo ngati khoma palamanja, ndi palamanzere. 23Ndipo Aaigupto anawalondola, nalowa pakati pa nyanja powatsata, ndiwo akavalo onse a Farao, magareta ace, ndi apakavalo ace. 24Ndipo kunali, ulonda wa

mamawa, Yehova ali m'moto ndi m'mtambo njo anapenyera pa ulendo wa
Aaigupto, Baubvuta ulendo wa Aaigupto. 25Ndipo anagurula njinga za
magareta ao, nawayendetsa molemetsa; pamenepo Aaigupto anati, Tithawe
pamaso pa Israyeli; pakuti Yehova alikuwagwirira nkhondo pa Aaigupto.

Aaigupto amizidwa m'nyanja

26Ndipo Yehova anati kwa Mose, Tambasulira dzanja lako kunyanja, kuti
madziwo abwerere kudzamiza Aaigupto, magareta ao, ndi apakavalo
ao. 27Ndipo Mose anatambasulira dzanja lace kunyanja, ndi nyanja inabwerera
m'mayendedwe ace mbanda kuca; ndipo Aaigupto pothawa anakomana nayo;
ndipo Yehova anakutumula Aaigupto m'kati mwa nyanja. 28Popeza madziwo
anabwerera, namiza magareta ndi apakavalo, ndiwo nkhondo yonse ya Farao
imene idalowa pambuyo pao m'nyanja; sanatsala wa iwowa ndi mmodzi
yense. 29Koma ana a Israyeli anayenda pouma pakati pa nyanja; ndi madziwo
anakhala ngati khoma kwa iwo, palamanja ndi palamanzere. 30Comweco
Yehova anapulumutsa Israyeli tsiku lomwelo m'manja a Aaigupto; ndipo Israyeli
anaona Aaigupto akufa m'mphepete mwa nyanja. 31Ndipo Israyeli anaiona
nchito yaikuru imene Yehova anacitira Aaigupto, ndipo anthuwo anaopa
Yehova; nakhulupirira Yehova ndi mtumiki wace Mose.

Eksodo 15
1Nyimbo yolemekeza Mulungu, Pamenepo Mose ndi ana a Israyeli anayimbira
Yehova nyimbo iyi, nanena, ndi kuti,
Ndidzayimbira Yehova pakuti wapambanatu;
Kavalo ndi wokwera wace anawaponya m'nyanja.
2Yehova ndiye mphamvu yanga ndi nyimbo yanga,
Ndipo wakhala cipulumutso canga;
Ameneyo ndiye Mulungu wanga, ndidzamlemekeza:
Ndiye Mulungu wa kholo langa, ndidzammveketsa.
3Yehova ndiye wankhondo;
Dzina lace ndiye Yehova.
4Magareta a Farao ndi nkhondo yace anawaponya m'nyanja;
Ndi akazembe ace osankhika anamira m'Nyanja Yofiira.
5Nyanja inawamiza:
Anamira mozama ngati mwala.
6Dzanja lanu lamanja, Yehova, lalemekezedwa ndi mphamvu,
Dzanja lanu lamanja, Yehova, laphwanya mdani.
7Ndipo ndi ukulu wanu waukuru mwapasula akuukira Inu;
Mwatumiza mkwiyo wanu, unawanyeketsa ngati ciputu.
8Ndipondi mpumo wa m'mphuno mwanu madzi anaunjikika,
Mayendedwe ace anakhala ciriri ngati mulu;
Zozama zinalimba m'kati mwa nyanja.
9Mdani anati,
Ndiwalondola, ndiwakumika, ndidzagawa zofunkha;
Ndidzakhuta nao mtima;
Ndidzasolola lupanga langa, dzanja langa lidzawaononga.
10Munaombetsa mphepo yanu, nyanja inawamiza;
Anamira m'madzi akuru ngati mtobvu.
11Manana ndi Inu ndani mwa milungu, Yehova?
Manana ndi Inu ndani, wolemekezedwa, woyera,
Woopsa pomyamika, wakucita zozizwa?
12Mwatambasula dzanja lanu lamanja,
Nthaka inawameza,
13Mwa cifundo canu mwatsogolera anthu amene mudawaombola;
Mwa mphamvu yanu mudawalondolera njira yakumka pokhala panu poyera.
14Mitundu ya anthu idamva, inanthunthumira;
Kuda mtima kwagwira anthu okhala m'Filistiya.
15Pamenepo mafumu a Edomu anadabwa;
Agwidwa nako kunthunthumira amphamvu a ku Moabu;
Okhala m'Kanani onse asungunukamtima.
16Kuopa kwakukuru ndi mantha ziwagwera;
Pa dzanja lanu lalikuru akhala cete ngati mwala;
Kufikira apita anthu anu, Yehova,
Kufikira apita anthu amene mudawaombola.
17Mudzawafikitsa, ndi kuwaoka pa phiri la colowa canu,
Pamalo pamene munadzipangira mukhalepo, Yehova,

Malo oyera, amene manja anu, Ambuye, adakhazikika.
18Yehova adzacita ufumu nthawi yomka muyaya.
19Pakuti akavalo a Farao analowa m'nyanja, ndi magareta ace ndi apakavalo ace, ndipo Yehova anawabwezera madzi a m'nyanja; koma ana a Israyeli anayenda pouma pakati pa nyanja. 20Ndipo Miriamu mneneriyo, mlongo wa Aroni, anagwira lingaka m'dzanja lace; ndipo akazi onse anaturuka kumtsata ndi malingaka ndi kuthira mang'ombe.
21Ndipo Miriamu anawayankha,
Yimbirani Yehova, pakuti wapambanatu;
Kavalo ndi wokwera wace anawaponya m'nyanja.
Madzi a ku Mara.
22Ndipo Mose anatsogolera Israyeli kucokera ku Nyanja Yofiira, ndipo anaturukako nalowa m'cipululu ca Suri; nayenda m'cipululu masiku atatu, osapeza madzi. 23Pamene anafika ku Mara, sanakhoza kumwa madzi a Mara, pakuti anali owawa; cifukwa cace anacha dzina lace Mara. 24Ndipo anthu anadandaulira Mose, ndi kuti, Tidzamwa ciani? 25Ndipo iye anapfuulira kwa Yehova; ndipo Yehova anamsonyeza mtengo ndipo anauponya m'madzimo, ndi madzi anasanduka okoma. Pamenepo anawapangira lemba ndi ciweruzo, ndi pomwepa anawayesa; 26ndipo anati, Ngati udzamveratu mau a Yehova, Mulungu wako, ndi kucita zoona pamaso pace, ndi kuchera khutu pa malamulo ace, ndi kusunga malemba ace onse, za nthenda zonse ndinaziika pa Aaigupto sindidzaziika pa iwe nnena imodzi; pakuti Ine Yehova ndine wakuciritsa iwe.
27Ndipo anafika pa Elimu, ndi pamenepo panali akasupe a madzi khumi ndi awiri, ndi akanjedza makumi asanu ndi awiri; ndipo anamanga cigono cao pomwepo pa madziwo.

Eksodo 16
Zinziri ndi mana
1Ndipo anacoka ku Elimu, ndi khamu lonse la ana a Israyeli linalowa m'cipululu ca Sini, ndico pakati pa Elimu ndi Sinai, tsiku lakhumi ndi cisanu la mwezi waciwiri ataturuka m'dziko la Aigupto. 2Ndipo khamu lonse la ana a Israyeli linadandaulira Mose ndi Aroni m'cipululu; 3nanena nao ana a Israyeli, Ha! mwenzi titafa ndi dzanja la Yehova m'dziko la Aigupto, pokhala ife pa miphika ya nyama, pakudya mkate ife cokhuta; pakuti mwatiturutsa kudza nafe m'cipululu muno kudzapha msonkhano uwu wonse ndi njala. 4Ndipo Yehova anati kwa Mose, Taona, ndidzabvumbitsira inu mkate wodzera kumwamba; ndipo anthu azituruka ndi kuola muyeso wa tsiku pa tsiku lace, kuti ndiwayese, ngati ayenda m'cilamulo canga kapena iai. 5Ndipo kudzakhala tsiku lacisanu ndi cimodzi, kuti azikonza umene adabwera nao, ataoniezapo muyeso unzace wa pa tsiku limodzi. 6Ndipo Mose ndi Aroni ananena ndi ana onse a Israyeli, Madzulo mudzadziwa kuti Yehova anakuturutsani m'dziko la Aigupto; 7ndi m'mawa mwace mudzaona ulemerero wa Yehova, popeza alinkumva mulikudandaulira Yehova; pakuti ife ndife ciani, kuti mutidandaulira ife? 8Nanenanso Mose, Pakukupatsani Yehova nyama ya kudya madzulo, ndi mkate wokhuta m'mawa, atero popeza Yehova adamva madandaulo anu amene mumdandaulira nao. Koma ife ndife ciani? simulikudandaulira ife koma Yehova. 9Ndipo Mose anati kwa Aroni, Nena ndi khamu lonse la ana a Israyeli, Yandikizani pamaso pa Yehova, pakuti anamva madandaulo anu. 10Ndipo kunakhala, pakunena Aroni ndi khamu lonse la ana a Israyeli kuti iwo anatembenukira kucipululu, ndipo, taonani, ulemerero wa Yehova unaoneka mumtambo. 11Ndipo Yehova ananena ndi Mose, ndi kuti, 12Ndamva madandaulo a ana a Israyeli; lankhula nao ndi kuti, Madzulo mudzadya nyama, ndi m'mawa mudzakhuta mkate; ndipo mudzadziwa kuti Ine ndine Yehova Mulungu wanu. 13Ndipo kunali madzulo zinakwera zinziri, ndipo zinakuta tsasa, ndi m'mawa padagwa mame pozungulira tsasa. 14Ndipo atasansuka mame adagwawo, taonani, pankhope pa cipululu pali kanthu kakang'ono kamphumphu, kakang'ono ngati cipale panthaka. 15Ndipo pamene ana a Israyeli anakaona, anati wina ndi mnzace, Nciani ici? pakuti sanadziwa ngati nciani. Ndipo Mose ananena nao, Ndiwo mkatewo Yehova wakupatsani ukhale cakudya canu, 16Amenewo ndiwo mau walamulira Yehova, Aoleko yense monga mwa njala yace; munthu mmodzi omeri limodzi, monga momwe muli, yense atengere iwo m'hema mwace. 17Ndipo ana a Israyeli anatero, naola wina wambiri, wina pang'ono. 18Ndipo pamene anayesa ndi omeri, iye amene adaola wambiri sunamtsalira, ndi iye amene adaola pang'ono sunamsowa; yense anaola monga mwa njala yace. 19Ndipo Mose ananena nao, Palibe munthu asiyeko kufikira m'mawa. 20Koma sanammvera Mose; ndipo ena anasiyako kufikira m'mawa; koma unagwa mphutsi, nununkha. Ndipo Mose anakwiya nao. 21Ndipo anauola m'mawa ndi m'mawa, yense monga mwa njala yace; popeza likatentha dzuwa umasungunuka. 22Ndipo kunali tsiku lacisanu ndi cimodzi, anaola mkate, naonjezapo linzace, maomeri awiri pa munthu mmodzi; ndipo akazembe a khamulo anadza nauza Mose. 23Ndipo ananena nao, Ici ndi comwe Yehova analankhula, Mawa ndiko kupuma, Sabata lopatulika la Yehova; cimene muzioca, ocani, ndi cimene muziphika phikani; ndi

cotsala cikukhalireni cosunguka kufikira m'mawa. 24Ndipo anausunga kufikira m'mawa, monga adalamulira Mose; koma sunanunkha, ndipo sunagwa mphutsi. 25Ndipo Mose anati, Muudye lero; pakuti lero ndilo Sabata la Yehova; simuupeza lero pabwalo. 26Muziola uwu masiku asanu ndi limodzi; koma tsiku lacisanu ndi ciwiri ndilo la Sabata, pamenepo padzakhala palibe. 27Ndipo kunali tsiku la Sabata, kuti anthu ena anaturuka kukaola, koma sanaupeza. 28Ndipo Yehova anati kwa Mose, Mukana kusunga zouza zanga ndi malamulo anga kufikira titi? 29Taonani, popeza Yehova anakupatsani Sabata, cifukwa cace tsiku lacisanu ndi cimodzi alikupatsa inu mkate wofikira masiku awiri; khalani yense m'malo mwace, munthu asaturuke m'malo mwace tsiku lacisanu ndi ciwiri. 30Ndipo anthu anapumula tsiku lacisanu ndi ciwiri. 31Ndipo mbumba ya Israyeli inaucha dzina lace Mana; ndiwo ngati zipatso zampasa, oyera; powalawa akunga timitanda tosanganiza ndi uci. 32Ndipo Mose anati, Awa ndi mau anauza Yehova, Dzazani omeri nao, asungikire mibadwo yanu; kuti aone mkatewo ndinakudyetsani nao m'cipululu, muja ndinakuturutsani m'dziko la Aigupto. 33Ndipo Mose anati kwa Aroni, Tenga mphika, nuthiremo mana odzala omeri, nuuike pamaso pa Yehova, usungikire mibadwo yanu. 34Monga Yehova anauza Mose, momwemo Aroni anauika patsogolo pa Mboni, usungikeko. 35Ndipo ana a Israyeli anadya mana zaka makumi anai, kufikira atalowa dziko la midzi; anadya mana kufikira analowa malire a dziko la Kanani. 36Koma omeri ndilo limodzi la magawo khumi la efa.

Eksodo 17

Madzi aturuka m'thanthwe ku Horebe

1Ndipo khamu lonse la ana a Israyeli linacoka m'cipululu ca Sini, m'zigono zao,
monga mwa mau a Yehova, nagona m'Refidimu. Koma kumeneko kunalibe
madzi akumwa anthu. 2Pamenepo anthu anatsutsana ndi Mose, nati, Tipatseni
madzi timwe, Koma Mose ananena nao, Mutsutsana nane bwanji? Muyeseranji
Yehova? 3Ndipo pomwepo anthu anamva ludzu lokhumba madzi; ndi anthu
anadandaulira Mose, nati, Munatikwezeranji kucokera ku Aigupto, kudzatipha
ife ndi ana athu ndi zoweta zathu ndi ludzu? 4Ndipo Mose anapfuulira kwa
Yehova, ndi kuti, Ndiwacitenji anthuwa? andilekera pang'ono kundiponya
miyala. 5Ndipo Yehova ananena ndi Mose, Pita pamaso pa anthu, nutenge
pamodzi nawe akuru ena a Israyeli; nutenge m'dzanja mwako ndodo ija
unapanda nayo nyanja, numuke. 6Taona, ndidzaima pamaso pako pathanthwe
m'Horebe; ndipo upande thanthwe, nadzaturukamo madzi, kuti anthu amwe.
Ndipo Mose anacita comweco pamaso pa akuru a Israyeli. 7Ndipo anacha
dzina la malowo Masa, ndi Meriba, cifukwa ca kutsutsana kwa ana a Israyeli;
popezanso anayesa Yehova, ndi kuti, Kodi Yehova ali pakati pa ife, kapena iai?

Aisrayeli apambana Amaleki

8Pamenepo anadza Amaleki, nayambana ndi Israyeli m'Refidimu. 9Ndipo Mose
anati kwa Yoswa, Utisankhulire amuna, nuturuke kuyambana naye Amaleki;
mawa ndidzaima pamwamba pa citunda, ndi ndodo ya Mulungu m'dzanja
langa. 10Ndipo Yoswa anacita monga Mose adanena naye, nayambana ndi
Amaleki; ndipo Mose, ndi Aroni, ndi Huri anakwera pamwamba pa
citunda. 11Ndipo kunakhala, pamene Mose anakweza dzanja lace Israyeli
analakika; koma pamene anatsitsa dzanja lace Amaleki analakika. 12Koma
manja a Mose analema; ndipo anatenga mwala, nauika pansi pa iye, nakhala
pamenepo; ndipo Aroni ndi Huri anagwiriziza manja ace, wina mbali yina, wina
mbali yina; ndi manja ace analimbika kufikira litalowa dzuwa. 13Ndipo Yoswa
anatyola Amaleki ndi anthu ace ndi kuukali kwa lupanga. 14Ndipo Yehova anati
kwa Mose, Lembera ici m'buku, cikhale cikumbutso, nucimvetse Yoswa; kuti
ndidzafafaniza konse cikumbukilo ca Amaleki pansi pa thambo. 15Ndipo Mose
anamanga guwa la nsembe, nalicha dzina lace Yehova Nisi: 16nati, Yehova
walumbira: padzakhala nkhondo ya Yehova pa Amaleki m'mibadwo mibadwo.

Eksodo 18

Yetero azonda Mose nampangira

1Ndipo Yetero, wansembe wa Midyani, mpongozi wa Mose, anamva zonse
zimene Mulungu adacitira Mose ndi Israyeli anthu ace, kuti Yehova adaturutsa
Israyeli m'Aigupto. 2Ndipo Yetero, mpongozi wa Mose, anabwera naye Zipora
mkazi wa Mose (atamtuma kwao), ndi ana ace awiri; 3dzina la winayo ndiye
Gerisomu, pakuti anati, Ndakhala mlendo m'dziko lacilendo; 4ndi dzina la
mnzace ndiye Eliezere; pakuti anati, Mulungu wa kholo langa anakhala
thandizo langa nandilanditsa ku lupanga la Farao. 5Ndipo Yetero, mpongozi wa
Mose, anadza ndi ana ace amuna ndi mkazi wace kwa Mose kucipululu
kumene adamangako, pa phiri la Mulungu; 6nati kwa Mose, Ine mpongozi wako
Yetero ndadza kwa iwe, ndi mkazi wako, ndi ana ace omwe awiri.
7Ndipo Mose anaturuka kukakomana ndi mpongozi wace, nawerama,
nampsompsona; nafunsana ali bwanji, nalowa m'hema. 8Ndipo Mose
anafotokozera mpongozi wace zonse Yehova adazicitira Farao ndi Aaigupto
cifukwa ca Israyeli; ndi mabvuto onse anakomana nao panjira, ndi kuti Yehova
adawalanditsa. 9Ndipo Yetero anakondwera cifukwa ca zabwino zonse Yehova
adazicitira Israyeli, ndi kuwalanditsa m'dzanja la Aaigupto. 10Nati Yetero,
Woyamikika Yehova, amene anakulanditsani m'dzanja la Aaigupto, ndi m'dzanja
la Farao; ameneanalanditsa anthu awa pansi pa dzanja la Aaigupto. 11Tsopano
ndidziwa kuti Yehova ali wamkuru ndi milungu yonse; pakuti momwe
anadzikuza okha momwemo anawaposa, 12Ndipo Yetero, mpongozi wa Mose,
anamtengera Mulungu nsembe Yopsereza, ndi nsembe zophera; ndipo Aroni
ndi akuru onse a Israyeli anadza kudzadya mkate ndi mpongozi wa Mose
pamaso pa Mulungu. 13Ndipo kunatero kuti m'mawa mwace Mose anakhala
pansi kuweruzira anthu mirandu yao; ndipo anthu anakhala ciriri pamaso pa
Mose kuyambira m'mawa kufikira madzulo. 14Ndipo pamene mpongozi wace
wa Mose anaona zonsezi iye anawacitira anthu, anati, Cinthu ici nciani
uwacitira anthuci? Umakhala pa wekha bwanji, ndi anthu onse amakhala ciriri
pamaso pako kuyambira m'mawa kufikira madzulo? 15Ndipo Moce anati kwa
mpongozi wace, Cifukwa anthu amadza kwa ine kudzafunsira
Mulungu; 16akakhala nao mlandu adza kwa ine, kuti ndiweruze pakati pa
munthu ndi mnansi wace, ndi kuti ndiwadziwitsemalemba a Mulungu, ndi
malamulo ace. 17Koma mpongozi wa Mose ananena naye, Cinthu ucitaci siciri
cabwino ai. 18Udzalema konse, iwe ndi anthu amene uli nao; pakuti cikulaka
cinthu ici; sungathe kucicita pa wekha. 19Tamvera mau anga tsopano,
ndikupangire nzeru, ndi Mulungu akhale nawe; ukhale m'malo mwa anthu kwa
Mulungu, nupite nayo mirandu kwa Mulungu; 20nuwamasulire malemba, ndi
malamulo, ndi kuwadziwitsa njira imene ayenera kuyendamo, ndi nchito imene
ayenera kucita. 21Koma iwe, dzisankhire mwa anthu ako onse, amuna amtima,
akuopa Mulungu, amuna oona, akudana nalo phindu la cinyengo; nuwaikire iwo
oterewa, akuru a pa zikwi, akuru a pa mazana, akuru a pa makumi asanu,
akuru a pa makumi; 22ndipo iwo aweruze mirandu ya anthu nthawi zonse;
ndipo kudzakhala kuti mirandu yaikuru yonse abwere nayo kwa iwe; koma
mirandu yaing'ono yonse aweruze okha; potero idzakucepera nchito, ndi iwo
adzasenza nawe. 23Ukacite cinthuci, ndi Mulungu akakuuza cotero, udzakhoza
kupirira, ndi anthu awa onse adzapita kwao mumtendere. 24Ndipo Mose

anamvera mau a mpongozi wace, nacita zonse adazinena. 25Ndipo Mose anasankha amuna amtima mwa Aisrayeli onse, nawaika akuru a pa anthu, akuru a pa zikwi, akuru a pa mazana, akuru a pa makumi asanu, ndi akuru a pa makumi. 26Ndipo anaweruza anthu nthawi zonse; mlandu wakuwalaka amabwera nao kwa Mose, ndi milandu yaing'ono yonse amaweruza okha. 27Ndipo Mose analola mpongozi wace amuke; ndipo anacoka kumka ku dziko lace.

Eksodo 19

Mulungu alamulira anthu za ku Sinai

1Mwezi wacitatu atataruka ana a Israyeli m'dziko la Aigupto, tsiku lomwelo,
analowa m'cipululu ca Sinai. 2Pakuti anacoka ku Refidimu, nalowa m'cipululu
ca Sinai, namanga tsasa m'cipululumo; ndipo Israyeli anamanga tsasa
pamenepo pandunji pa phirilo. 3Ndipo Mose anakwera kwa Mulungu; ndipo
Yehova ali m'phirimo anamuitana, ndi kuti, Uzitero kwa mbumba ya Yakobo,
nunene kwa ana a Israyeli, kuti, 4Inu munaona cimene ndinacitira Aaigupto; ndi
kuti ndanyamula inu monga pa mapiko a mphungu, ndi kubwera nanu kwa Ine
ndekha. 5Ndipo tsopano, ngati mudzamvera mau anga ndithu, ndi kusunga
cipangano canga, ndidzakuyesani cuma canga ca padera koposa mitundu
yonse ya anthu; pakuti dziko lonse lapansi ndi langa; 6ndipo ndidzakuyesani
ufumu wanga wa ansembe, ndi mtundu wopatulika. Awa ndi mau amene
ukalankhule ndi ana a lsrayeli. 7Ndipo Mose anadza, naitana akuru a anthu,
nawaikira pamaso pao mau awa onse amene Yehova adamuuza. 8Ndipo anthu
onse anabvomera pamodzi, nati, Zonse adazilankhula Yehova tidzazicita. Ndipo
Mose anabwera nao mau a anthu kwa Yehova. 9Ndipo Yehova anati kwa Mose,
Taona, ndikudza kwa iwe mu mtambo wakuda bii, kuti anthu amve pamene
ndilankhula ndi iwe, ndi kuti akubvomereze nthawi zonse. Pakuti Mose adauza
Yehova mau a anthuwo. 10Ndipo Yehova anati kwa Mose, Muka kwa anthuwo,
nuwapatulitse lero ndi mawa, ndipo atsuke zobvala zao, 11nakonzekeretu tsiku
lacitatu; pakuti tsiku lacitatu Yehova adzatsika pa phiri la Sinai pamaso pa anthu
onse. 12Ndipo ukalembere anthu malire pozungulira, ndi kuti, Muzicenjera
musakwere m'phiri, musakhudza cilekezero cace; wokhudza phirilo
adzaphedwa ndithu; 13dzanja liri lonse lisalikhudze, wakulikhudza azimponyatu
miyala, kapena kumpyoza; ngakhale coweta ngakhale munthu, zisakhale ndi
moyo. Pamene lipenga libanika liu lace azikwera m'phirimo. 14Ndipo Mose
anatsika m'phiri kumka kwa anthu, nawapatulitsa anthu; natsuka iwo zobvala
zao. 15Ndipo anati kwa anthu, Mukonzekeretu tsiku lacitatu nimusayandikiza
mkazi. 16Ndipo kunali tsiku lacitatu, m'mawa, panali mabingu ndi zimphezi, ndi
mtambo wakuda bii paphiripo, ndi liu la lipenga lolimbatu; ndi anthu onse okhala
kutsasa ananjenjemera. 17Ndipo Mose anaturutsa anthu kutsasa, kuti akomane
ndi Mulungu; ndipo anaima patsinde pa phiri. 18Ndipo phiri la Sinai linafuka
monsemo, popeza Yehova anatsikira m'moto pamenepo; ndi utsi wace
unakwera ngati utsi wa m'ng'anjo, ndi phiri lonse linagwedezeka
kwambiri, 19Ndipo pamene liu la lipenga linamveka linakulira-kulira, Mose
ananena, ndi Mulungu anamyankha ndi mau. 20Ndipo Yehova anatsikira pa
phiri la Sinai, pamutu pace pa phiri; ndipo Yehova anaitana Mose akwere
pamutu pa phiri; ndi Mose anakwerapo. 21Ndipo Yehova anati kwa Mose, Tsika,
cenjeza anthu, kuti angapyolere kwa Yehova kudzaona, ndipo angagwe ambiri
a iwowa. 22Ansembenso, akuyandikiza kwa Yehova adzipatulitse,
angawapasule Yehova. 23Ndipo Mose anati kwa Yehova, Anthu sangathe
kukwera m'phiri la Sinai; pakuti Inu mwaticenjeza, ndi kuti, Lemba malire
m'phirimo, ndi kulipatula. 24Ndipo Yehova anati kwa iye, Muka, tsika: nukwere
iwe ndi Aroni pamodzi ndi iwe; koma ansembe ndi anthu asapyole kukwera kwa
Yehova, angawapasule. 25Pamenepo Mose anawatsikira anthu, nanena nao.

Eksodo 20

Malamulo khumi a Mulungu

1Ndipo Mulungu ananena mau onse amenewa, nati:
2INE ndine YEHOVA Mulungu wako, amene ndinaturutsa iwe ku dziko la Aigupto, ku nyumba ya akapolo.
3Usakhale nayo milungu yina koma Ine ndekha.
4Usadzipangire iwe wekha fano losema, kapena cifaniziro ciri conse ca zinthu za m'thambo la kumwamba, kapena za m'dziko lapansi, kapena za m'madzi a pansi pa dziko; 5usazipembedzere izo, usazitumikire izo; cifukwa Ine Yehova Mulungu wako ndiri Mulungu wansanje, wakulanga ana cifukwa ca atate ao, kufikira mbadwo wacitatu ndi wacinai wa iwo amene akudana ndi Ine; 6ndi kuwacitira cifundo anthu zikwizikwi a iwo amene akondana ndi Ine, nasunga malamulo anga.
7Usaehule dzina la Yehova Mulungu wako pacabe; cifukwa Yehova sadzamuyesa iye wosacimwa, amene achula pacabe dzina lacelo.
8Uzikumbukila tsiku la Sabata, likhale lopatulika. 9Masiku asanu ndi limodzi uzigwira, ndi kumariza nchito zako zonse; 10koma tsiku lacisanu ndi ciwiri ndilo Sabata la Yehova Mulungu wako; usagwire nchito iri yonse, kapena iwe wekha, kapena mwana wako wamwamuna, kapena mwana wako wamkazi, kapena wanchito wako wamwamuna, kapena wanchito wako wamkazi, kapena nyama zako, kapena mlendo amene ali m'mudzi mwako; 11cifukwa masiku asanu ndi limodzi Yehova adamariza zakumwamba ndi zapansi, ndi nyanja, ndi zinthu zonse ziri m'menemo, napumula tsiku ladsanu ndi ciwiri; cifukwa cace Yehova anadalitsa tsiku la Sabata kuti likhale lopatulika.
12Uzilemekeza atate wako ndi amako; kuti acuruke masiku ako m'dziko limene Yehova Mulungu wako akupatsa iwe.
13Usaphe.
14Usacite cigololo.
15Usabe.
16Usamnamizire mnzako.
17Usasirire nyumba yace ya mnzako, usasirire mkazi wace wa mnzako, kapena wanchito wace wamwamuna, kapena wanchito wace wamkazi, kapena ng'ombe yace, kapena buru wace, kapena kanthu kali konse ka mnzako.
18Ndipo anthu onse anaona mabingu ndi zimphezi, ndi liu la lipenga, ndi phiri lirikufuka; ndipo pamene anthu anaziona, ananjenjemera, naima patali. 19Ndipo anati kwa Mose, Mulankhule nafe ndinu, ndipo tidzamva; koma asalankhule nafe Mulungu, kuti tingafe, 20Ndipo Mose anati kwa anthu, Musaope; pakuti Mulungu wadza kukuyesani ndi kuti kumuopa iye kukhale pamaso panu, kuti musacimwe. 21Ndipo anthu anaima patali, koma Mose anayandikiza ku mdima waukuru kuli Mulungu.

Za mafano ndi guwa la nsembe

22Ndipo Yehova anati kwa Mose, Uzitero ndi ana a Israyeli, kuti, Mwapenya nokha kuti ndalankhula nanu, kucokerakumwamba. 23Musapange milungu yasiliva ikhale pamodzi ndi Ine; musadzipangire milungu yagolidi. 24Undiumbire guwa la nsembe ladothi, nundiphere pomweponsembe zako zopsereza, ndi nsembe zako zamtendere, nkhosa zako ndi ng'ombe zako; pali ponse ndikumbukiritsa anthu dzina langa ndidzakudzera ndi kukudalitsa. 25Ndipo

ukandimangira guwa la nsembe lamiyala, usalimanga ndi miyala yosema;
ukakwezapo cosemera cako, waliipsa. 26Kapena usakwere ndi makwerero ku
guwa langa la nsembe, kuti angaoneke marisece ako pamenepo.

Eksodo 21

Lamulo la pa kapolo, ndi la pa wakupha mnzace

1Ndipo awa ndiwo maweruzo amene uziika pamaso pao.
2Ukagula mnyamata Mhebri, azigwira nchito zaka zisanu ndi cimodzi; koma cacisanu ndi ciwiri azituruka waufulu cabe. 3Akalowa ali yekha azituruka ali yekha; akakhala ndi mkazi, mkazi wace azituruka naye. 4Akampatsa mkazi mbuye wace, ndipo akambalira ana amuna ndi akazi, mkaziyo ndi ana ace azikhala a mbuye wace, ndipo azituruka ali yekha. 5Koma mnyamatayo akanenetsa, Ndikonda mbuye wanga, mkazi wanga, ndi ana anga; sindituruka waufulu; 6pamenepo mbuye wace azifika naye kwa oweruza, nafike naye kukhomo, kapena kumphuthu, ndipo mbuye wace amboole khutu lace ndi lisungulu; ndipo iye azimgwirira nchito masiku onse.
7Ndipo munthu akagulitsa mwana wace wamkazi akhale mdzakazi, iyeyo asaturuke monga amaturuka anyamata. 8Akapanda kumkonda mbuye wace, amene anamtoma mwini yekha, azilola kuti amuombole; alibe mphamvu yakumgulitsa kwa anthu acilendo, popeza wacita naye monyenga. 9Koma ngati amtomera mwana wace wamwamuna, amcitire monga kuyenera ana akazi. 10Akamtengera mkazi wina, asacepetse cakudya cace, zobvala zace, ndi za ukwati zace zace. 11Ndipo akapanda kumcitira izi zitatu, azituruka cabe, osaperekapo ndalama.
12Iye amene akantha munthu kotero kuti wafa, aphedwe ndithu. 13Koma akapanda kumlalira, koma Mulungu akalola akomane ndi mnzace, ndidzakuikirani pothawirapo iye. 14Koma munthu akacita dala pa mnzace, kumupha monyenga; uzimcotsa ku guwa langa la nsembe, kuti afe.
15Munthuwakukanthaatatewace, kapena amai wace, aphedwe ndithu.
16Iye wakuba munthu, angakhale wamgulitsa, kapena akampeza m'dzanja lace, aphedwe ndithu.

Malamulo a pa wotemberera ombala ndi opweteka anzao

17Munthu wakutemberera atate wace, kapena amai wace, aphedwe ndithu.
18Akalimbana amuna, ndipo wina akakantha mnzace ndi mwala, kapena ndi nkhonyo, wosafa iye, koma wakhulungira pakama; 19akaukanso, nakayendayenda pabwalo ndi ndodo yace, womkanthayo azikhala womasuka; pakutsotsa pace pokha azimbwezera, namcizitse konse.
20Munthu akakantha mnyamata wace, kapena mdzakazi wace, ndi ndodo, ndipo akafa padzanja pace; ameneyo aliridwe ndithu. 21Koma akakhala wosafa tsiku limodzi kapena awiri, asalirike, pakuti ndiye ndalama ya mbuye wace.
22Akayambana amuna, nakakantha mkazi ali ndi pakati, kotero kuti abala, koma alibe kuphwetekwa; alipe ndithu, monga momwe amchulira mwamuna wa mkaziyo; apereke monga anena oweruza. 23Koma ngati kuphweteka kukalipo, uzipereka moyo kulipa moyo, 24diso kulipa diso, dzino kulipa dzino, dzanja kulipa dzanja, phazi kulipa phazi, 25kutentha kulipa kutentha, bala kulipa bala, mkwapulo kulipa mkwapulo.
26Munthu akampanda mnyamata wace, kapena mdzakazi wace, padiso, nalithudzula, azimlola amuke waufulu cifukwa ca diso lace. 27Ndipo akagurula dzino la mnyamata wace, kapena dzino la mdzakazi wace, azimlola amuke waufulu cifukwa ca dzino lace.

28Ng'ombe ikatunga mwamuna kapena mkazi, nafa, aiponyetu miyala ng'ombeyo, osadya nyama yace; koma mwini ng'ombeyo azimasuka. 29Koma ngati ng'ombe ikatunga masiku adapitawo, ndipo anamcenjeza mwiniyo, koma osaisunga iye, ndipo ikapha mwamuna kapena mkazi, aiponye miyala ng'ombeyo, ndi mwini waceyo amuphenso. 30Akamuikira dipo, azipereka ciombolo ca moyo wace monga mwa zonse adamuikira. 31Ingakhale yatunga mwana wamwamuna kapena wamkazi, aicitire monga mwa ciweruzo ici. 32Ng'ombeyo ikatunga mnyamata kapena mdzakazi, azipatsa mbuye wace ndalama za masekele a siliva makumi atatu, ndipo ng'ombeyo aiponye miyala.

Malamulo a pa cuma

33Munthu akafukula dzenje, kapena akakumba dzenje, osalibvundikira, ndipo ikagwamo ng'ombe kapena buru, 34mwini dzenje azilipa; azilipa ndalama kwa mwini nyamayo, koma yakufayo ndi yace.

35Ng'ombe ya mwini ikapweteka ng'ombe ya mnzace, nifa, azigulitsa ng'ombe yamoyoyo, nagawe ndalama zace; naigawe, ndi yakufa yomweyo. 36Kapena kudadziwika kuti ng'ombeyo ikatunga masiku adapitawo, koma osaisunga mwiniyo, azilipa ndithu, ng'ombe kulipa ng'ombe, koma yakufayo ndi yace.

1Munthu akaba ng'ombe, kapena nkhosa, nakaipha, kapena kuigulitsa, azilipa
ng'ombe zisanu pa ng'ombeyo; ndi nkhosa zinai pa nkhosayo, 2Akampeza
wakuba alimkuboola, nakamkantha kotero kuti wafa, palibe
camwazi. 3Litamturukira dzuwa, pali camwazi; wakubayo azilipa ndithu; ngati
alibe kanthu, amgulitse pa umbala wace. 4Akacipeza cakubaco ciri m'dzanja
lace camoyo, ngakhale ng'ombe, kapena buru, kapena nkhosa, alipe mowirikiza.
5Munthu akadyetsa coweta pabusa kapena pa munda wamphesa, atamasula
coweta cace, ndipo citadya podyetsa pa mwini wace; alipe podyetsa pace
poposa, ndi munda wa mphesa wace woposa.
6Ukayaka moto, nukalandira kuminga, kotero kuti unyeketsa mulu wa tirigu,
kapena tirigu wosasenga, kapena munda; woyatsa motoyo alipe ndithu.
7Munthu akaikiza ndalama kapena cuma kwa mnansi wace, ndipo zibeka
m'nyumba ya munthuyo; akapeza mbala, ilipe cowirikiza. 8Akapanda kumpeza
mbalayo, abwere naye mwini nyumbayo kwa oweruza, kumuyesa ngati anaika
dzanja lace pa cuma ca mnansi wace. 9Mlandu uti wonse wa colakwa, kunena
za ng'ombe, za buru, za nkhosa, za cobvala, za kanthu kali konse kotayika,
munthu anenako kali kace; mlandu wa onse awiri ufike kwa oweruza; iye
amene oweruza amtsutsa alipe cowirikiza kwa mnansi wace.
10Munthu akaikiza buru, kapena ng'ombe, kapena nkhosa, kapena coweta cina
kwa mnansi wace, ndipo cikafa, kapena ciphwetekwa, kapena wina acipitikitsa
osaciona munthu; 11lumbiro la Yehova likhale pakati pa iwo awiri, kuti
sanaturutsa dzanja lace pa cuma ca mnansi wace; ndipo mwiniyo
azibvomereza, ndipo asalipe. 12Koma ngati cidabedwa kwaoko ndithu, alipe
kwa mwiniyo. 13Ngati cajiwa ndithu, abwere naco cikhale mboni; asalipe pa
cojiwaco.
14Munthu akabwereka cinthu kwa mnansi wace, ndipo ciphwetekwa, kapena
cifa, mwiniyo palibe, azilipa ndithu. 15Akakhalapo mwiniyo, asalipe; ngati
cagwirira nchito yakulipira, cadzera kulipira kwace.

Malamulo osiyana a pakati pa anthu

16Munthu akanyenga namwali wosapalidwa ubwenzi, nakagona nave, alipetu
kuti akhale mkazi wace. 17Atate wace akakana konse kumpatsa iye, alipe
ndalama monga mwa colipa ca anamwali.
18Wanyanga usamlola akhale ndi moyo.
19Ali yense agona ndi coweta aphedwe ndithu.
20Wakuphera nsembe mulungu wina, wosati Yehova yekha, aonongeke
konse. 21Ndipo usasautsa mlendo kapena kumpsinja; pakuti munali alendo
m'dziko la Aigupto. 22Musazunza mkazi wamasiye, kapena mwana wamasiye
ali yense. 23Ukawazunza ndi kakuti konse, nakandilirira pang'ono ponse
iwowa, ndidzamvadi kulira kwao; 24ndi mkwiyo wanga idzayaka, ndipo
ndidzapha inu ndi lupanga; ndipo akazi anu adzakhala amasiye, ndi ana anu
omwe.
25Ukakongoletsa ndalama anthu anga osauka okhala nanu, usamkhalira ngati
wangongole; usamwerengera phindu. 26Ukati ulandire cikole kaya cobvala ca
mnansi wako, koma polowa dzuwa ucibwezere kwa iye; 27popeza copfunda
cace ndi ici cokha, ndico cobvala ca pathupi pace; azipfundira ciani pogona?

Ndipo kudzakhala kuti akandipfuulira Ine, ndidzamva; pakuti Ine ndine wacisomo.
28Usapeputsa oweruza, kapena kutemberera mkuru wa anthu a mtundu wako. 29Usacedwa kuperekako zipatso zako zocuruka, ndi zothira zako. Woyamba wa ana ako amuna undipatse Ine. 30Uzitero nazo ng'ombe zako, ndi nkhosa zako; masiku asanu ndi atatu akhale ndi amai wace; tsiku lacisanu ndi citatu uzimpereka kwa Ine. 31Ndipo muzindikhalira Ine anthu opatulika; cifukwa cace musamadya nyama yojiwa kuthengo; itayireni agaru.

Eksodo 23

Za mabodza ndi zonyenga

1Usatola mbiri yopanda pace; usathandizana naye woipa ndi kukhala mboni
yocititsa ciwawa. 2Usatsata unyinji wa anthu kucita coipa; kapena usacita
umboni kumlandu, ndi kupatukira kutsata unyinji ndi kukhotetsa
mlandu; 3kapena usakometsera munthu wosauka pa mlandu wace.
4Ukakomana ndi ng'ombe kapena buru wa mdani wako zirimkusokera,
uzimbwezera izo ndithu. 5Ukaona buru wa munthuwakudana nawe alikugona
pansi ndi katundu wace, ndipo ukadaleka kuthandiza, koma uzimthandiza
ndithu.
6Usakhotetsa mlandu wa mnzako waumphawi. 7Uzikhala kutali ndi mlandu
wonama; ndipo usapha munthu wosacimwa ndi wolungama; pakuti
sindidzayesa wolungama munthu woipa. 8Usalandira cokometsera mlandu;
pakuti cokometsera mlandu cidetsa maso a openya, nicisanduliza mlandu wa
olungama, 9Usampsinia mlendo; pakuti mudziwa mtima wa mlendo popeza
munali alendo m'dziko la Aigupto.

Za nthawi zopumula

10Ndipo uzibzala m'munda mwako zaka zisanu ndi cimodzi, ndi kututa zipatso
zako; 11koma caka cacisanu ndi ciwiri uuleke, ugone; kuti aumphawi a anthu a
mtundu wako adyemo ndipo zotsalira iwowa zoweta za kubusa zizidye;
momwemo uzicita ndi munda wako wamphesa,
ndimundawakowaazitona. 12Uzicita nchito yako masiku asanu ndi limodzi,
koma tsiku lacisanu ndi ciwiri uzipumula; kuti ng'ombe yako ndi buru wako
zipumule, ndi kuti mwana wa mdzakaziwako ndi mlendo atsitsimuke. 13Ndipo
samalirani zonse ndanena ndi inu; nimusachule dzina la milungu yina;
lisamveke pakamwa pako.

Za madyerero atatu m'caka

14Muzindicitira loe madyerero katatu m'caka. 15Uzisunga madyerero a mkate
wopanda cotupitsa; masiku asanu ndi awiri uzidya mkate wopanda cotupitsa,
monga ndinakuuza, nyengo yoikika, mwezi wa Abibu, pakuti m'menemo
unaturuka m'Aigupto; koma asaoneke munthu pamaso panga opanda
kanthu; 16ndi madyerero a masika, zipatso zoyamba za nchito zako, zimene
udazibzala m'munda; ndi madyerero a kututa, pakutha caka, pamene ututa
nchito zako za m'munda. 17Katatu m'caka amuna onse azioneka pamaso pa
Ambuye Yehova.
18Usapereka mwazi wa nsembe yanga pamodzi ndi mkate wacotupitsa; ndi
mafuta a madyerero anga asagonamo kufikira m'mawa. 19Uzibweca nazo
zoyambayamba za m'munda mwako ku nyumba ya Yehova Mulungu wako.
Usaphike mwana wa mbuzi mu mkaka wa mace.
Mulungu aloniezana nao za Kanani. 20Taona, ndituma mthenga akutsogolere,
kukusunga panjira, ndi kukufikitsa pamalo pomwe ndakonzeratu. 21Musamalire
iye, ndi kumvera mau ace; musamwawitsa mtima, pakuti sadzakhululukira zoo
lakwa zanu; popeza dzina langa liri m'mtima mwace. 22Pakuti ukamveratu mau
ace, ndi kucita zonse ndizilankhula, ndidzakhala mdani wa adani ako, ndipo
ndidzasautsa akusautsa iwe. 23Pakuti mthenga wanga adzakutsogolera,
nadzakufikitsa kwa Aamori, ndi Ahiti, ndi Aperizi, ndi Akanani, Ahivi, ndi Ayebusi;
ndipo ndidzawaononga. 24Usagwadira milungu yao, kapena kuwatumikira,

kapena kucita monga mwa nchito zao; koma uwapasule konse, ndi kugamulatu zoimiritsa zao. 25Ndipo muzitumikira Yehova Mulungu wanu, potero adzadalitsa cakudya cako, ndi madzi ako; ndipo ndidzacotsa nthenda pakati pa iwe. 26M'dziko mwanu simudzakhala wakutaya mwana, kapena wosabala; ndidzakwaniritsa kuwerenga kwa masiku ako. 27Ndidzatumiza kuopsa kwanga kukutsogolere, ndipo ndidzapitikitsa anthu onse amene udzafika kwao, ndipo ndidzacita kuti adani ako onse adzakuonetsa m'mbuyo mwao. 28Ndipo ndidzatumiza mabvu akutsogolere amene adzaingitsa Ahivi, Akanani, ndi Ahiti, pamaso pako. 29Sindidzawaingista pamaso pako caka cimodzi; kuti dziko lingakhale bwinja, ndi zirombo za kuthengo zingakucurukire. 30Ndidzawaingitsa pang'ono pang'ono pamaso pako, kufikira utacuruka, ndi kulandira dziko colowa cako. 31Ndipo ndidzalemba malire ako kuyambira ku Nyanja Yofiira, kufikira ku nyanja ya Afilisiti, ndi kuyambira kucipululu kufikira ku Nyanja; popeza ndidzapereka okhala m'dzikolo m'dzanja lako, ndipo uziwaingitsa pamaso pako. 32Usapangana nao, kapena ndi milungu yao. 33Asakhale m'dziko lako iwowa, kuti angakulakwitse pa loe; pakuti ukatumikira milungu yao, kudzakukhalira msampha ndithu.

Eksodo 24

Mose ndi akuru akwera m'phiri

1Ndipo iye ananena ndi Mose, Ukwere kudza kwa Yehova, iwe ndi Aroni, Nadabu ndi Abihu, ndi akuru a Israyeli makumi asanu ndi awiri; ndipo mugwadire pakudza kutali; 2ndipo Mose yekha ayandikire kwa Yehova; koma asayandikire iwowa; ndi anthunso asakwere naye. 3Ndipo Mose anadza nafotokozera anthu mau onse a Yehova, ndi masveruzo onse; ndipo anthu onse anabvomera pamodzi, nati, Mau onse walankhula Yehova tidzacita. 4Ndipo Mose analembera mau onse a Yehova, nalawira kuuka mamawa, namanga guwa la nsembe patsinde pa phiri, ndi zoimiritsa khumi ndi ziwiri, kwa mafuko khumi ndi awiri a Israyeli. 5Ndipo anatuma ana a Israyeli a misinkhu ya anyamata, ndiwo anapereka nsembe zopsereza, naphera Yehova nsembe zamtendere, zang'ombe. 6Ndipo Mose anagawa mwaziwo, nathira wina m'zotengera, nawaza wina pa guwa la nsembe. 7Ndipo anatenga buku la Cipangano, nawerenga m'makutu a anthu; ndipo iwo anati, Zonse zimene Yehova walankhula tidzacita, ndi kumvera. 8Ndipo Mose anatenga mwaziwo, nawaza pa anthu, nati, Taonani mwazi wa cipangano, cimene Yehova anacita nanu, kunena za mau awa onse, 9Ndipo Mose ndi Aroni, Nadabu ndi Abihu, ndi akuru a Israyeli makumi asanu ndi awiri anakwerako; 10ndipo anapenya Mulungu wa Israyeli; ndipo pansi pa mapazi ace panali ngati mayalidwe oyera a miyala yasafiri, ndi ngati thupi la thambo loti mbe. 11Koma sanaturutsa dzanja lace pa akuru a ena a Israyeli; ndipo anapenya Mulungu, nadya, namwa. 12Ndipo Yehova anati kwa Mose, Ukwere kudza kwa Ine m'phiri muno, nukhale pompano; ndipo ndidzakupatsa magome amiyala, ndi cilamulo ndi malamulo, ndawalembera kuti uwalangize. 13Ndipo anauka Mose, ndi Yoswa mtumiki wace; ndipo Mose anakwera m'phiri la Mulungu. 14Ndipo anati kwa akuru, Tilindeni kuno kufikira tidzabwera kwa inu; ndipo taonani, Aroni ndi Huri ali nanu; munthu akakhala ndi mlandu abwere kwa iwowa. 15Ndipo Mose anakwera m'phirimo, ndi mtambo unaphimba phirilo, 16Ndipo ulemerero wa Yehova unakhalabe pa phiri la Sinai, ndi mtambo unaliphimba masiku asanu ndi limodzi; ndipo tsiku lacisanu ndi ciwiri iye ali m'kati mwa mtambo anaitana Mose. 17Ndipo maonekedwe a ulemerero wa Yehova anali ngati mota wonyeketsa pamwamba pa phiri, pamaso pa ana a Israyeli. 18Ndipo Mose analowa m'kati mwa mtambo, nakwera m'phirimo; ndipo Mose anakhala m'phiri masiku makumi anai usana ndi usiku.

Eksodo 25

Zopereka zaufulu zakumanga Malo Opatulika

1Ndipo Yehova ananena ndi Mose, ndi kuti, 2Lankhula ndi ana a Israyeli, kuti
anditengere copereka; ulandire copereka canga kwa munthu ali yense mtima
wace umfunitsa mwini. 3Ndipo coperekaco ucilandire kwa iwo ndi ici: golidi, ndi,
siliva, ndi mkuwa, 4ndi lamadzi, ndi: lofiirira, ndi lofiira, ndi bafuta wa thonje
losansitsa, ndi ubweya wa mbuzi; 5ndi zikopa za nkhosa zamphongo zonika
zofiira, ndi zikopa za akatumbu, ndi mtengo wasitimu; 6mafuta akuunikira,
zonunkhira za mafuta odzoza, ndi za cofukiza ca pfungo lokoma; 7miyala
yaberulo, ndi miyala yoika paefodi, ndi pacapacifuwa. 8Ndipo andimangire malo
opatulika; kuti ndikhale pakati pao, 9Monga mwa zonse Ine ndirikuonetsa iwe,
cifaniziro ca kacisi, ndi cifaniziro ca zipangizo zace zonse, momwemo
ucimange.

Za likasa, cotetezerapo, ndi akerubi

10Ndipo azipanga likasa la mtengo wasitimu: utali wace mikono iwiri ndi hafu,
kupingasa kwace mkono ndi hafu, msinkhu wace mkono ndi hafu. 11Ndipo
ulikute ndi golidi woona, ulikute m'kati ndi kubwalo, nulipangire mkombero
wagolidi pozungulira pace. 12Ndipo uliyengere mphete zinai zagolidi, ndi
kuziika ku miyendo yace inai; mphete ziwiri pa mbali yace yina, ndi mphete
ziwiri pa yina. 13Ndipo uzipanga mphiko za mtengo wasitimu, ndi kuzikuta ndi
golidi. 14Nupise mphiko m'mphetezo pa mbali zace za likasa, zakunyamulira
nazo likasalo. 15Mphiko zikhale m'zimphete za likasa; asazisolole. 16Ndipo
uziika m'likasamo mboni imene ndidzakupatsa. 17Ndipo uzipanga cotetezerapo
ca golidi woona; utali wace mikono iwiri ndi hafu, ndi kupingasa kwace mkono
ndi hafu. 18Uzipanganso akerubi awiri agolidi; uwasule mapangidwe ace, pa
mathungo ace awiri a cotetezerapo. 19Nupange kerubi mmodzi ku thungo lino,
ndi kerubi wina ku thungo lina; upange akerubi ocokera kucotetezerapo, pa
mathungo ace awiri. 20Ndipo akerubi afunyululire mapiko ao m'mwamba, ndi
kuphimba cotetezerapo ndi mapiko ao, ndi nkhope zao zipenyane; nkhope za
akerubi ziphenye kucotetezerapo, 21Ndipo uziika cotetezerapo pamwamba pa
likasa, ndi kuikamo mboni ndidzakupatsayo m'likasamo. 22Ndipo pomwepo
ndidzakomana ndi iwe, ow kulankhula ndi iwe, ndiri pamwamba pa
cotetezerapo, pakati pa akerubi awiriwo okhala pa likasa la mboni, zonse
zimene ndidzakuuza za ana a Israyeli.

Za gome la mkate woonekera

23Ndipo uzipanga gome la mtengo wasitimu; utali wace mikono iwiri, ndi
kupingasa kwace mkono umodzi, ow msinkhu wace mkono ndi hafu. 24Ndipo
ulikute ndi golidi woona ndi kulipangira mkombero wagolidi pozungulira
pace. 25Nulipangire mitanda pozungulirapo yoyesa cikhato m'kupingasa
kwace, ndi pamitanda pace pozungulira upangirepo mkombero
wagolidi. 26Nulipangire mphete zinai zagolidi, ndi kuika mphetezo pa ngondya
zinai zokhala pa miyendo yace inai. 27Mphetezo zikhale pafupi pa mitanda,
zikhale zopisamo mphiko za kunyamulira nazo gome. 28Ndipo uzipanga
mphiko za mtengo wasitimu, ndi kuzikuta ndi golidi, kuti anyamulire nazo
gome. 29Ndipo uzipanga mbale zace, ndi zipande zace, ndi mitsuko yace, ndi
zikho zace zakuthira nazo; uzipanga za golidi woona. 30Ndipo uziikamkate
woonekera pa gomelo pamaso panga nthawi zonse.

Za coikapo nyali

31Ndipo uzipanga coikapo nyali ca golidi woona; coikapoco cisulidwe
mapangidwe ace, tsinde lace ow thupi lace; zikho zace, mitu yace, ndi maluwa
ace zikhale zocokera m'mwemo; 32ndipo m'mbali zace muturuke mphanda
zisanu ndi imodzi; mphanda zitatu za coikapo nyalico zituruke m'mbali yace
yina, ndi mphanda zitatu za coikapo nyalico zituruke m'mbali inzace. 33Ku
mphanda yina kukhale zikho zitatu zopangika ngati katungurume, mutu ndi
luwa; ndi ku mphanda inzace zikho zitatu zopangika ngati katungurume, mutu
ndi luwa; zitere mphanda zisanu ndi imodzi zoturuka m'coikapo
nyalico. 34Ndipo pa coikapo nyali comwe pakhale zikho zinai zopangika ngati
katungurume, mitu yace ndi maluwa ace; 35pakhale mutu pansi pa mphaada
ziwiri zoturuka m'mwemo, ndi mutu pansi pa mphanda ziwiri zoturuka
m'mwemo, ndi mutu pansi pa mphanda ziwiri zoturuka m'mwemo; itere ku
mphanda zisanu ndi imodzi zoturuka m'coikapo nyalico. 36Mitu yao ndi
mphanda zao zikhale zoturuka m'mwemo; conseci cikhale cosulika cimodzi ca
golidi woona. 37Ndipo uzipanga nyali zace, zisanu ndi ziwiri; ndipo ayatse nyali
zace, ziwale pandunji pace. 38Ndipo mbano zace, ndi zoolera zace, zikhale za
golidi woona. 39Acipange ici ndi zipangizo izi zonse za talente wa golidi
woona. 40Ndipo uyang'anire uzipanga monga mwacifaniziro cao, cimene
anakuonetsa m'phirimo.

Eksodo 26

Kacisi ndi nsaru zophimba zace

1Ndipo uzipanga kacisi ndi nsaru zophimba khumi, za bafuta wa thonje losansitsa, ndi thonje lamadzi, ndi lofiirira, ndi lofiira; uombemo akerubi, nchito ya mmisiri. 2Utali wace wa nsaru yophimba imodzi ndiwo mikono makumi awiri kudza isanu ndi itatu, ndi kupingasa kwa nsaru imodzi ndiko mikono inai; nsaru zonse zikhale za muyeso umodzi. 3Nsaru zisanu zilumikizane yina ndi inzace; ndi nsaru zisanu zina zilumikizane yina ndi inzace. 4Ndipo uziika magango a nsaru yamadzi m'mphepete mwace mwa nsaru imodzi, ku mkawo wa cilumikizano; nucite momwemo m'mphepete mwace mwa nsaru ya kuthungoya cilumikizano dna. 5Uziika magango makumi asanu pa nsaru yocingira imodzi, nuikenso magango makumi asanu m'mphepete mwace mwa nsaru ya cilumikizano cina; ndipo magango akomanizane lina ndi linzace. 6Uzipanganso zokowera makumi asanu zagolidi, ndi kumanga nsaruzo pamodzi ndi zokowerazo; kuti kacisi akhale mmodzi. 7Ndipo uziomba nsaru zophimba za ubweya wa mbuzi zikhale hema pamwamba pa kacisi; uziomba nsaru khumi ndi imodzi. 8Utali wace wa nsaru imodzi ndiwo mikono makumi atatu, ndi kupingasa kwace kwa nsaru imodzi ndiko mikono inai; nsarukhumi ndi imodzi zikhale za muyeso womwewo. 9Nuzisoka pamodzi nsaru zisanu pa zokha ndi nsaru zisanu ndi imodzi pa zokha, nupinde nsaru yacisanu ndi cimodziyo pa khomo la hema. 10Ndipo uziika magango makumi asanu m'mphepete mwa nsaru imodzi, ya kuthungo ya cilumikizano, ndi magango makumi asanu m'mphepete mwa nsaru ya kuthungo ya cilumikizano cina. 11Ndipo uzipanga zokowera makumi asanu zamkuwa, ndi kukowetsa zokowerazo m'magangomo, ndi kumanga pamodzi hemalo likhale limodzi. 12Ndipo cotsalaco pa nsaru za hemalo, hafu yace ya nsaru yotsalirayo, icinge pambuyo pace pa kacisi. 13Ndi mkono wa pa mbali yino, ndi mkono wa pa mbali inzace, wakutsalira m'utali wace wa nsaru za hemalo, icinge pambali zace za kacisi, mbali yino ndi mbali yina, kumphimba. 14Ndipo uzipangira hema cophimba ca zikopa za nkhosa zamphongo zonika zofiira, ndi cophimba za zikopa za akatumbu pamwamba pace.

Za matabwa oimirika a kacisi

15Ndipo uzipangira kacisi matabwa oimirika, a mtengo wasitimu. 16Utali wace wa thabwa limodzi ndiwo mikono khumi, ndi kupingasa kwace kwa thabwali mkono ndi hafu. 17Pa thabwa limodzi pakhale mitsukwa iwiri, yomangika pamodzi; uzitero pa matabwa onse a kacisi. 18Ndipo uzipanga matabwa a kacisi, matabwa makumi awiri ku mbali ya kumwela, kumwela. 19Nuzipanga makamwa makumi anai asiliva pansi pa matabwa makumi awiri; makamwa awiri pansi pa thabwa limodzi kwa mitsukwa yace iwiri, ndi makamwa awiri pansi pa thabwa lina kwa mitsukwa yace iwiri; 20ndi pa mbali yace yina ya kacisi, mbali ya kumpoto, pakhale matabwa makumi awiri; ndi makamwa asiliva makumi anai; 21makamwa awiri pansi pa thabwa limodzi, ndi makamwa awiri pansi pa thabwa lina. 22Ndipo uzipanga matabwa asanu ndi limodzi kwa mbali ya kacisi ya kumbuyo kumadzulo. 23Nupange matabwa awiri a ngondya za kacisi za kumbuyo. 24Ndipo akhale ophatikizika pamodzi patsinde, nakhalenso ophatikizika pamodzi kumutu kwace ndi mphete imodzi; azitero onse awiri; azikhala a ngondya ziwiri. 25Ndipo pakhale matabwa asanu ndi atatu, ndi

makamwa ao asiliva, ndiwo makamwa khumi mphambu asanu ndi limodzi;
makamwa awiri pansi pa thabwa limodzi, ndi makamwa awiri pansi pa thabwa
lina. 26Ndipo uzipanga mitanda ya mtengo wasitimu; isanu ya matabwa a pa
mbali yina ya kacisi, 27ndi mitanda isanu ya matabwa a Pel mbali yina ya
kacisi, ndi mitanda isanu ya matabwa a pa mbali ya kacisi ya kumbuyo
kumadzulo. 28Ndi mtanda wa pakati pa matabwa ufikire kuthungo. 29Ndipo
uzikuta matabwa ndi golidi, ndi kupanga mphete zao zagolidi zopisamo
mitandayo; uzikutanso mitandayo ndi golidi. 30Ndipo uutse kacisi monga mwa
makhalidwe ace amene anakusonyeza m'phiri.

Za nsaru yosiyanitsa ya pakhomo

31Ndipo uziomba nsaru yocinga ya thonje lamadzi, ndi lofiirira ndi lofiira, ndi la
bafuta wa thonje losansitsa, aiombe ndi akerubi nchito ya mmisiri; 32ndipo
uicinge pa mizati inai ya mitengo wasitimu, zokuta ndi golidi; zokowera zao
zikhale zagolidi, ndi makamwa anai asiliva. 33Ndipo uzicinga nsaru yocinga pa
zokowerazo, nulowetse likasa la mboni kukati kwa nsaru yocinga; ndipo nsaru
yocingayo idzakugawirani pakati pa malo opatulika ndi malo
opatulikitsa. 34Ndipo uziika cotetezerapo pa likasa la mboni, m'malo
opatulikitsa. 35Nuziika gomelo kunja kwa nsaru yocinga, ndi coikapo nyali
pandunji pa gome, pa mbali ya kumwela ya kacisi; koma uike gomelo pa mbali
ya kumpoto, 36Ndipo uziomba nsaru yotsekera pa khomo la bema, ya lakuda,
ndi lofiirira, ndi lofiira, ndi bafuta wa thonje losansitsa, nchito ya
wopikula. 37Ndipo uzipangira nsaru yotsekerayo nsanamira zisanu za mtengo
wasitimu, ndi kuzikuta ndi golidi; zokowera zao zikhale zagolidi; nuziyengera
makamwa asanu amkuwa.

Eksodo 27

Za guwa la nsembe

1Ndipo upange guwa la nsembe la mtengo wasitimu, utali wace mikono isanu,
ndi kupingasa kwace mikono isanu, guwa la nsembelo likhale lampwamphwa,
ndi msinkhu wace mikono itatu. 2Ndipo uzipanga nyanga zace pa ngondya
zace zinai; nyanga zace zikhale zoturuka m'mwemo: nulikute ndi
mkuwa: 3Ndipo uzipanga zotayira zace zakulandira mapulusa ace, ndi zoolera
zace, ndi mbale zowazira zace, ndi mitungo yace, ndi zoparira moto zace;
zipangizo zace zonse uzipanga zamkuwa. 4Ndipo ulipangire made, malukidwe
ace ndi amkuwa; nupange pa malukidwewo ngondya zace zinai mphete zinai
zamkuwa. 5Nuwaike pansi pa matso a guwa la nsembelo posungulira, kuti
malukidwe alekeze pakati pa guwa la nsembelo. 6Ndipo upangire guwa la
nsembe mphiko, mphiko za mtengo wasitimu, ndi kuzikuta ndi mkuwa. 7Ndipo
apise mphiko m'mphetezo kuti mphikozo zikhale pa mbali ziwiri za guwa la
nsembe polinyamula. 8Ulipange lagweregwere ndi matabwa; monga
anakuonetsa m'phirimo; alipange momwemo.

Za bwalo la cihema

9Upangenso bwalo la cihema; pa mbali yace ya kumwela, kumwela, pakhale
nsaru zocingira zakubwaloza nsaru ya bafuta wa thonje losansitsa, utali wace
wa pa mbali imodzi mikono zana; 10ndi nsici zace makumi awiri, ndi makamwa
ao makumi awiri akhale amkuwa; zokowera za nsici ndi mitanda yace zikhale
zasiliva. 11Momwemonso pa mbali ya kumpoto m'utali mwace pakhale nsaru
zocingira za mikono zana limodzi m'utali mwace; ndi nsici zace makumi awiri,
ndi makamwa ao akhale amkuwa; zokowera za nsicizo ndi mitanda yace
zikhale zasiliva. 12Ndipo m'kupingasa kwa bwaloli pa mbali ya kumadzulo
mukhale nsaru zocingira za mikono makumi asanu; nsici zace zikhale khumi,
ndi makamwa ao khumi. 13Ndipo m'kupingasa kwace kwa bwalo pa mbali ya
kum'mawa, kum'mawa, mukhale mikono makumi asanu. 14Ndi nsaru zocingira
za pa mbali imodzi ya kucipata zikhale za mikono khumi ndi isanu; nsici zace
zikhale zitatu, ndi makamwa ao atatu. 15Ndi pa mbali yina pakhale nsaru
zocingira za mikono khumi ndi isanu; nsici zace zikhale zitatu, ndi makamwa ao
atatu. 16Ndipo pa cipata ca bwalolo pakhale nsaru yotsekera ya mikono
makumi awiri, ya lamadzi ndi lofiirira, ndi lofiira, ndi bafuta wa thonje losansitsa,
nchito ya wopikula; nsici zace zikhale zinai, ndi makamwa ao anai. 17Nsici
zonse za pabwalo pozungulira zimangike pamodzi ndi mitanda yasiliva;
zokowera zao zasiliva, ndi makamwa ao amkuwa. 18Utali wace wa bwalolo
ukhale wa mikono zana limodzi, ndi kupingasa kwace makumi asanu monsemo,
ndi msinkhu wace wa mpanda mikono isanu; ukhale wabafuta wa thonje
losansitsa; ndi makamwa a nsicizo akhale amkuwa. 19Zipangizo zonse za
kacisi, m'macitidwe ace onse, ndi ziciri zace zonse, ndi ziciri zonse za bwalo
lace, zikhale zamkuwa.

Za mafuta a nyaliyo

20Ndipo uuze ana a Israyeli akutengere mafuta a azitona oyera opera
akuunikira, kuti awalitse nyali kosalekeza. 21Aroni ndi ana ace aikonze
m'cihema cokomanako, kunja kwa nsaru yocinga yokhala kumboni, kuyambira
madzulo kufikira m'mawa; likhale lemba losatha mwa mibadwo yao, alisunge
ana a Israyeli.

Eksodo 28

Za zobvala zopatulika

1Ndipo akuyandikire Aroni mbale wako, ndi ana ace amuna pamodzi naye,
mwa ana a Israyeli, kuti andicitire Ine nchito ya nsembe, ndiwo Aroni, Nadabu,
ndi Abihu, Eleazara ndi Itamara, ana a Aroni. 2Ndipo usokere Aroni mbale wako
zobvala zopatulika, zikhale zaulemerero ndi zokoma. 3Ndipou lankhule ndi
onse a mtima waluso, amene ndawadzaza ndi mzimu waluso, kuti amsokere
Aroni zobvala apatulidwe nazo, andicitire Ine nchito ya nsembe. 4Ndipo zobvala
azisoka ndizi: capacifuwa ndi efodi, ndi mwinjiro, ndi malaya opikapika, ndi
nduwira, ndi mpango; tero apangire Aroni mbale wako ndi ana ace zobvala
zopatulika, kuti andicitire Ine nchito ya nsembe, 5Ndipo atenge golidi, ndi
lamadzi ndi lofiirira ndi lofiira, ndi bafuta wa thonje losansitsa.

Za Efodi

6Naombe efodi ndi golidi, ndi lamadzi, ndi lofiirira, ndi lofiira ndi bafuta wa
thonje losansitsa, nchito ya mmisiri. 7Akhale nazo zapamapewa ziwiri
zomangika ku nsonga zace ziwiri, kuti amangike nazo. 8Ndipo mpango wa
efodi, wokhala pamenepo, kuti ammange nao, ukhale wa ciombedwe comweco,
ndi woombera kumodzi, wagolidi, ndi thonje lamadzi, ndi lofiirira ndi lofiira, ndi
bafuta wa thonje losansitsa. 9Ndipo utenge miyala iwiri yaberulo, nulocepo
maina a ana a Israyeli; 10maina asanu ndi limodzi pa mwala wina, ndi maina
asanu ndi limodzi otsala pa mwala unzace, mwa kubadwa kwao. 11Uloce
miyala iwiriyo ndi maina a ana a Israyeli, monga mwa nchito ya woloca miyala,
monga malembedwe a cosindikizira, uipange igwirike ndi zoikamo
zagolidi, 12Ndipo ulike miyala iwiriyo pa zapamapewa za efodi, ikhale miyala ya
cikumbutso ca ana a Israyeli; ndipo Aroni azinyamula maina ao pa mapewa ace
awiri, akhale cikumbutso pamaso pa Yehova.
13Ndipo upange zoikamo za golidi; 14ndi maunyolo awiri a golidi woona;
uwapote ngati zingwe, nchito yopota; numange maunyolo opotawo
pazoikamo. 15Upangenso capacifuwa ca ciweruzo, nchito ya mmisiri; uciombe
mwa ciombedwe ca efodi; uciombe ndi golidi, lamadzi, ndi lofiirira, ndi lofiira, ndi
bafuta wa thonje losansitsa. 16Cikhale campwamphwa, copindika, utali wace
cikhato cimodzi, ndi kupingasa kwace cikhato cimodzi. 17Ndipo uikepo miyala
yoikikapo, mizere inai ya miyala; mzere wa odemu, pitida, ndi bareketi, ndiyo ya
mzere woyamba; 18ndi mzere waciwiri wa nofeki, safiri, ndi yahaloni; 19ndi
mizere wacitatu wa lesemu, sibu, ndi akalama; 20ndi mzere wacinai wa tarisisi,
sohamu, ndi yasefe; zikhale zogwirika ndi golidi m'zoikamo zao. 21Ndi miyalayi
ikhale monga mwa maina a ana a Israyeli, khumindiawiri, monga maina ao;
monga malocedwe a cosindikizira, yonse ikhale monga maina ao, kwa mafuko
khumi ndi awiri. 22Upangenso maunyolo pa capacifuwa ngati zingwe, nchito
yopota, ya golidi woona. 23Nupangire pa capacifuwa mphete ziwiri zagolidi, ndi
kuzika mphete ziwirizo pa nsonga zace ziwiri za capacifuwa. 24Numange
maunyolo awiri opota agolidi ku mphete ziwiri pansonga pace pa
capacifuwa. 25Koma nsonga zace ziwiri za maunyolo opotawo uzimange ku
zoikamo ziwiri, ndi kuziika pa zapamapewa ziwiri za efodi, m'tsogolo
mwace. 26Ndipo upange mphete ziwiri zagolidi, ndi kuzimanga pa nsonga zace
ziwiri za capacifuwa, m'mphepete mwace, m katimo ku mbali ya
kuefodi. 27Upangenso mphete ziwiri zagolidi, ndi kuzimanga pa zapamapewa

ziwiri za efodi, m'munsi, ku mbali yace ya kutsogolo, pafupi pa msoko wace, pamwamba pa mpango wa efodi. 28Ndipo amange capacifuwa pa mphete zace ndi mphete za efodi ndi mkuzi wamadzi, kuti cikhale pa mpango wa efodi; ndi kuti capacifuwa cisamasuke paefodi, 29Ndipo Aroni azinyamula maina a ana a Israyeli pa capacifuwa ca ciweruzo pamtima pace, pakulowa iye m'malo opatulika, akhale cikumbutso pankhope pa Yehova kosalekeza. 30Ndipo uike Urimu ndi Tumimu mwa capacifuwa ca ciweruzo; ndipo zikhale pa mtima wa Aroni, pakulowa iye pamaso pa Yehova; ndipo Aroni azinyamula ciweruzo ca ana a Israyeli pamtima pace pamaso pa Yehova kosalekeza.
31Ndipo uombe mwinjiro wa efodi ndi lamadzi lokha. 32Ndipo polowa mutu pakhale pakati pace; pakhale mkawo pozungulira polowa pace, wa nchito yoomba, ngati polowa pa malaya ociniiriza, pangang'ambike. 33Ndipo pa mbinyiru wace upange makangaza a lamadzi, ndi lofiirira, ndi lofiirira, pambinyiru pace pozungulira, ndi kuwapakiza ndi miliu yagolidi pozungulira; 34mliu wagolidi ndi khangaza, mliu wagolidi ndi khangaza, pa mbinyiru wa mwinjiro pozungulira. 35Ndipo Aroni aubvale kuti atumikire nao; ndipo limveke liu lace pakulowa iye m'malo opatulika pamaso pa Yehova, ndi pakuturuka iye, kuti asafe.

Za golidi waphanthiphanthi

36Ndipo upange golidi waphanthiphanthi woona, ndi kulocapo, monga malocedwe a cosindikizira. KUPATULIKIRA YEHOVA. 37Nuciike pamkuzi wamadzi, ndipo cikhale panduwira, cikhale patsogolo pace pa nduwira. 38Ndipo cizikhala pamphumi pace pa Aroni, ndipo Aroni azinyamula mphulupulu ya zopatulidwa, zimene ana a Israyeli azipatulira, ndi zopereka zao zonse zopatulira; ndipo cizikhala pamphumi pace kosalekeza, kuti alandiridwe pamaso pa Yehova. 39Ndipo upikule maraya am'kati abafuta a thonje losansitsa, nusoke nduwira wabafuta, nusokenso mpango wopikapika. 40Ndipo usokere ana a Aroni maraya am'kati, nuwasokere mipango; uwasokerenso akapa akhale aulemerero ndi okoma. 41Ndipo ubveke nazo Aroni mbale wako, ndi ana ace omwe; ndi a kuwadzoza, ndi kudzaza dzanja lao, ndi kuwapatula, andicitire Ine nchito ya nsembe. 42Uwasokerenso zobvala za miyendo za bafuta wa thome losansitsa kubisa marisece ao; ziyambire m'cuuno zifikire kuncafu. 43Ndipo azibvale Aroni, ndi ana ace, pakulowa iwo ku cihema cokomanako, kapena poyandikiza iwo ku guwa la nsembe kutumikira m'malo opatulika; anganyamule mphulupulu, nangafe; likhale lemba losatha la iye ndi mbumba zace pambuyo pace.

Eksodo 29

Mapatulidwe a ansembe

1Ici ndico uwacitire kuwapatula, andicitire nchito ya nsembe: tenga ng'ombe yamphongo, ndi nkhosa ziwiri zamphongo zangwiro, 2ndi mkate wopanda cotupitsa, ndi timitanda topanda cotupitsa tosanganiza ndi mafuta, ndi timitanda taphanthi topanda cotupitsa, todzoza ndi mafuta; utipange ndi ufa wosalala watirigu. 3Ndipo uziike mu mtanga umodzi, ndi kubwera nazo mumtanga, pamodzi ndi ng'ombe yamphongo ndi nkhosa ziwiri zamphongo. 4Ndipo ubwere nao Aroni ndi ana ace amuna ku khomo la cihema cokomanako indi kuwasambitsa m'madzi. 5Pamenepo utenge zobvalazo ndi kubveka Aroni maraya am'kati, ndi mwinjiro wa efodi, ndi efodi, ndi capacifuwa, ndi kummangira m'cuuno ndi mpango wa efodi woluka mwanzeru; 6ndipo uike nduwira pamutu pace, ndi kuika korona wopatulika panduwirapo. 7Pamenepo utenge mafuta odzoza nao nuwatsanulire pamutu pace, ndi kumdzoza. 8Ndipo ubwere nao ana ace amuna ndi kuwabveka maraya am'kati. 9Uwamangirenso Aroni ndi ana ace amuna mipango m'cuuno mwao, nuwamangire akapa pamutu pao; ndipo akhale ansembe mwa lemba losatha; nudzaze dzanja la Aroni ndi dzanja la ana ace amuna, 10Ndipo ubwere nayo ng'ombe yamphongo patsogolo pa cihema cokomanako; ndipo Aroni ndi ana ace amuna aike manja ao pamutu pa ng'ombe yamphongoyo. 11Nuphe ng'ombe yamphongoyo pamaso pa Yehova, pa khomo la cihema cokomanako. 12Pamenepo utapeko pa mwazi wa ng'ombe yamphongo, ndi kuupaka pa nyanga za guwa la nsembe ndi cala cako, nutsanulire mwazi wonse pa tsinde la guwa la nsembe. 13Nutenge mafuta onse akukuta matumbo, ndi cokuta ca mphafa ndi imso ziwiri, ndi mafuta ali pa izo, ndi kuzitentha pa guwa la nsembe. 14Koma nyama ya ng'ombeyo, ndi cikopa cace, ndi cipwidza cace, uzitentha izi ndi moto kunja kwa cigono; ndiyo nsembe yaucimo. 15Utengenso nkhosa yamphongo imodziyo; ndi Aroni ndi ana ace amuna aike manja ao pamutu pa nkhosa yamphongoyo. 16Nuiphe nkhosa yamphongoyo, ndi kutenga mwazi wace, ndi kuuwaza pa guwa la nsembe pozungulira. 17Ndipo upadzule nkhosa yamphongo m'ziwalo zace, ndi kutsuka matumbo ace, ndi miyendo yace, ndi kuziika pa ziwalo zace, ndi pamutu pace. 18Pamenepo upsereze, nkhosa yamphongo yonse pa guwa la nsembe; ndiyo nsembe yopsereza ya Yehova, ya pfungo lokoma; ndiyo nsembe yamoto ya Yehova. 19Ndipo utenge nkhosa yamphongo yinayo; ndi Aroni ndi ana ace amuna aike manja ao pamutu pa nkhosa yamphongoyo. 20Pamenepo uiphe nkhosa yamphongoyo, nutapeko pa mwazi wace, ndi kuupaka pa ndewerere ya khutu lamanja la Aroni, ndi pa ndewerere ya khutu lamanja la ana ace amuna, ndi pa cala cacikulu ca dzanja lao lamanja, ndi pa cala cacikulu ca phazi lao lamanja, ndi kuuwaza mwaziwo pa guwa la nsembe posungulira, 21Ndipo utapeko pamwazi uli pa guwa la nsembe, ndi pa mafuta akudzoza nao, ndi kuwaza pa Aroni, ndi pa zobvala zace, ndi pa ana ace amuna, ndi pa zobvala za ana ace amuna, pamodzi ndi iye; kuti akhale wopatulidwa, ndi zobvala zace zomwe, ndi ana ace amuna ndi zobvala zao zomwe pamodzi ndi iye. 22Utengenso mafuta a nkhosa yamphongoyo, ndi me ira, ndi mafuta akukuta mat umbo, ndi cokuta ca mphafa, ndi imso ziwiri, ndi mafuta ali pamenepo, ndi mwendo wam'mwamba wa ku dzanja lamanja; pakuti ndiyo nkhosa yamphongo ya kudzaza manja; 23ndi

mkate wamphumphu umodzi, ndi kamtanda ka mkate wosanganiza ndi mafuta, ndi kamtanda kamodzi kaphanthi, ziri mu mtanga wa mkate wopanda cotupitsa wokhala pamaso pa Yehova; 24ndipo uike zonsezo m'manja a Aroni, ndi m'manja a ana ace amuna; nuziweyule nsembe yoweyula pamaso pa Yehova. 25Pamenepo uzilandire m'manja mwao, ndi kuzipsereza pa guwa la nsembe, pa nsembe yopsereza, zicite pfungo lokoma pamaso pa Yehova; ndiyo nsembe yamoto ya Yehova. 26Ndipo utenge nganga ya nkhosa yamphongo yodzaza manja ya Aroni, ndi kuiweyula ikhale nsembe yoweyula pamaso pa Yehova; ndipo ikhale gawo lako. 27Ndipo upatule nganga va nsembe yoweyula, ndi mwendo wam'mwamba wa nsembe yokweza, imene anaiweyula, ndi imene anaikweza, za nkhosa yamphongo yakudzaza manja; ziri za Aroni, ndi za ana ace amuna; 28ndipo zikhale za Aroni ndi za ana ace amuna, mwa lemba losatha, ziwadzere kwa ana a Israyeli; popeza ndiyo nsembe yokweza; ndipo ikhale nsembe yokweza yodzera kwa ana a Israyeli, ya kwa nsembe zamtendere zao, ndiyo nsembe yao yokweza ya Yehova. 29Ndipo zobvala zopatulika za Aroni zikhale za ana ace amuna pambuyo pace, kuti awadzoze atazibvala, nadzaze manja ao atazibvala; 30mwana wace wamwamuna amene adzakhala wansembe m'malo mwace azibvala masiku asanu ndi awiri, pakulowa iye m'cihema cokomanako kutumikira m'malo opatulika. 31Ndipo utenge nkhosa yamphongo yodzaza manja, nuphike nayama yace m'malo opatulika. 32Ndipo Aroni ndi ana ace amuna adye nyama ya nkhosa yamphongoyo, ndi mkate uli mumtanga, pa khomo la cihema cokomanako. 33Ndipo adye zimene anacita nazo coteteza, kuti awadzaze manja ndi kuwapatulitsa; koma mlendo asadyeko, pakuti nzopatulika izi. 34Ndipo ikatsalako nyama yodzaza manja, kapena mkate kufikira m'mawa, pamenepo utenthe zotsalazo ndi moto; asazidye popeza ncopatulika ici. 35Ndipo utero nao Aroni, ndi ana ace amuna, monga mwa zonse ndakuuza; udzaze manja ao masiku asanu ndi awiri. 36Nukonze ng'ombe yamphongo, ndiyo nsembe yaucimo yakuteteza nayo, tsiku ndi tsiku; ndipo uyeretsa guwa la nsembe, pakucita coteteza pamenepo; ndipo ulidzoze kulipatula. 37Ucitire guwa la nsembe coteteza masiku asanu ndi awiri ndi kulipatula; ndipo a guwa la nsembelo likhale lopatulikitsa; ciri conse cikhudza guwa la nsembelo cikhale copatulika.

Nsembe ya masiku onse

38Koma izi ndizo uzikonza pa guwa la nsembelo; ana a nkhosa awiri a caka cimodzi, tsiku ndi tsiku kosalekeza. 39Mwana wa nkhosa wina ukonze m'mawa; ndi mwana wa nkhosa wina ukonze madzulo; 40ndi pa mwana wa nkhosa mmodziyo pakhale limodzi la magawo khumi la ufa wosalala, wosanganiza ndi limodzi la magawo anai la hini wa mafuta opera; ndi limodzi la magawo anai la hini wa vinyo, likhale nsembe yothira. 41Ndi mwana wa nkhosa wina ukonze madzulo; umkonze umo unacitira copereka ca m'mawa ndi nsembe yace yothira, akhale pfungo lokoma, nsembe yamoto ya Yehova. 42Ikhale nsembe yopsereza yosalekeza ya mwa mibadwo yanu, pa khomo la cihema cokomanako, pamaso pa Yehova, kumene ndidzakomana nanu, kulankhula nawe komweko. 43Ndipo pamenepo ndidzakomana ndi ana a Israyeli; ndipo cihema cidzapatulidwa ndi ulemerero wanga. 44Ndipo ndidzapatula cihema

cokomanako, ndi guwa la nsembe; ndidzapatulanso Aroni ndi ana ace amuna omwe, andicitire nchito ya nsembe. 45Ndipo ndidzakhala pakati pa ana a Israyeli, ndi kukhala Mulungu wao. 46Ndipo adzadziwa kuti Ine ndine Yehova Mulungu wao, amene ndinawaturutsa m'dziko la Aigupto, kuti ndikhale pakati pao. Ine ndine Yehova Mulungu wao.

Eksodo 30

Za guwa la nsembe lofukizapo

1Ndipo upange guwa la nsembe la kufukizapo; ulipange la mtengo
wasitimu. 2Utali wace ukhale mkono, ndi kupingasa kwace mkono; likhale
lampwamphwa; ndi msinkhu wace mikono iwiri; nyanga zace zituruke
m'mwemo. 3Ndipo ulikute ndi golidi woona, pamwamba pace ndi mbali zace
zozungulira, ndi nyanga zace; ulipangirenso mkombero wagolidi
pozungulira, 4Ndipo ulipangire mphete ziwiri zagolidi pansi pa mkombero wace;
uziike pa nthiti zace ziwiri, pa mbali zace ziwiri; zikhale zopisamo mphiko
kulinyamula nazo. 5Ndipo upange mphiko za mtengo wasitimu, ndi kuzikuta ndi
golidi. 6Nuliike cakuno ca nsaru yocinga iri ku likasa la mboni, patsogolo pa
cotetezerapo ciri pamwamba pa mboni, pomwe ndidzakomana ndi iwe. 7Ndipo
Aroni azifukizapo cofukiza ca zonunkhira zokoma m'mawandim'mawa, pamene
akonza nyalizo, acifukize. 8Ndipo pamene Aroni ayatsa nyalizo madzulo,
acifukize cofukiza cosatha pamaso pa Yehova mwa mibadwo
yanu, 9Musafukizapo cofukiza cacilendo, kapena nsembe yopsereza, kapena
copereka; musathirepo nsembe yothira. 10Ndipo Aroni azicita coteteza pa
nyanga zace kamodzi m'caka; alicitire coteteza ndi mwazi wa nsembe yaucimo
ya coteteza, mwa mibadwo yanu; ndilo lopatulikitsa la Yehova.

Ndarama za ciombolo

11Ndipo Yehova ananena ndi Mose, ndi kuti, 12Pamene uwerenga ana a
Israyeli, monga mwa mawerengedwe ao, munthu yense apereke kwa Yehova
ciombolo ca pa moyo wace, pa kuwerengedwa iwowa; kuti pasakhale mliri
pakati pao, pakuwerengedwa iwowa. 13Ici acipereke, yense wakupita kwa
owerengedwa; limodzi la magawo awiri a sekeli, monga sekeli la malo
opatulika; (sekeli ndilo magera makumi awiri) limodzi la magawo awiri a sekeli,
ndilo copereka ca Yehova. 14Yense wakupita kwa owerengedwawo, wa zaka
makumi awiri ndi wa mphambu zace, apereke coperekaco kwa
Yehova. 15Wacuma asacurukitsepo, ndi osauka asacepse pa limodzi mwa
magawo awiri a sekeli, pakupereka copereka kwa Yehova, kucita coteteza ca
miyoyo yanu. 16Ndipo uzilandira ndarama za coteteza kwa ana a Israyeli, ndi
kuzipereka pa nchito ya cihema cokomanako; kuti zikhale cikumbutso ca ana a
Israyeli pamaso pa Yehova, kucita coteteza ca miyoyo yanu.

Za mkhate wakusambiramo

17Ndipo Yehova analankhula ndi Mose, ndi kuti, 18Upangenso mkhate
wamkuwa, ndi tsinde lace lamkuwa, wakusambiramo; nuuike pakati pa ciliema
cokomanako ndi guwa la nsembe, ndi kuthiramo madzi. 19Ndipo Aroni ndi ana
ace amuna azisambiramo manja ao ndi mapazi ao; 20pakulowa iwo m'cihema
cokomanako asambe ndi madzi, kuti angafe; kapena poyandikiza guwa la
nsembe kutumikirako, kufukiza nsembe yamoto ya Yehova; 21asambe manja
ao ndi mapazi ao, kuti angafe: liwakhalire lemba losatha, kwa iye ndi kwa mbeu
zace, mwa mibadwo yao.

Za mafuta odzoza opatulika

22Yehova ananenanso ndi Mose, ndi kuti, 23Udzitengerenso zonunkhira
zomveka, mure woyenda masekeli mazana asanu, ndi kinimani lonunkhira
limodzi mwa magawo awiri a mureyo, ndilo masekeli mazana awiri kudza
makumi asanu, ndi kane lonunkhira mazana awiri kudza makumi asanu, 24ndi

kida mazana asanu, monga sekeli la malo opatulika, ndi mafuta a azitona hini limodzi; 25ndipo ukonze nazo mafuta odzoza opatulika, osanganizika monga mwa macitidwe a wosanganiza; akhale mafuta odzoza opatulika. 26Ndipo udzoze nao cihema cokomanako, ndi likasa la mboni, 27ndi gomelo ndi zipangizo zace zonse, ndi coikapo nyali ndi zipangizo zace, 28ndi guwa la nsembe lofukizapo, ndi guwa la nsembe yopsereza ndi zipangizo zace zonse, ndi mkhate wosambiramo ndi tsinde lace. 29Ndipo uzipatule, kuti zikhale zopatulika ndithu; zonse zakuzikhudza zidzakhala zopatulika. 30Ndipo udzoze Aroni ndi ana ace amuna, ndi kuwapatula andicitire nchito ya nsembe. 31Nulankhule ndi ana a Israyeli, ndi kuti, Awa ndi mafuta odzoza opatulika a Ine mwa mibadwo yanu. 32Asawatsanulire pa thupi la munthu; kapena musakonza ena onga awa, mwa makonzedwe ace; awa ndiwo opatulika, muwayese opatulika. 33Ali yense amene akonza ena otere, kapena ali yense awaika pa mlendo, ameneyo asazidwe kwa anthu a mtundu wace.

Za cofukiza

34Ndipo Yehova anati kwa Mose, Udzitengere zonunkhira, natafi, ndi sekeleti, ndi kelebuna; zonunkhira pamodzi ndi libano loona; miyeso yofanana; 35ndipo uzikonza nazo cofukiza, cosanganiza mwa macitidwe a wosanganiza, cokometsera ndi mcere, coona, copatulika; 36nupere cina cisalale, nuciike cakuno ca mboni m'cihema cokomanako, kumene ndidzakomana ndi iwe; uciyese copatulika ndithu. 37Koma za cofukizaco ucikonze, musadzikonzere nokha cina, mwa makonzedwe ace amene; muciyese copatulika ca Yehova. 38Ali yense wokonza cina cotere kununkhizapo, asadzidwe kwa anthu a mtundu wace.

1Za amisiri opanga nchitoyi, Ndipo Yehova ananena ndi Mose, ndi kuti, 2Taona
ndaitana ndi kumchula dzina lace, Bezaleli, mwana wa Uri, mwana wa Huri, wa
pfuke la Yuda; 3ndipo ndamdzaza nd mzimu wa Mulungu, ndi luso, ndi nzeru,
ndi cidziwitso, ndi m'nchito ziri zonse, 4kulingirira nchito zaluso, kucita ndi golidi
ndi siliva ndi mkuwa, 5ndi kuzokota miyala yoikika, ndi kuzokota mtengo, kucita
nchito ziri zonse. 6Ndipo Ine, taona, ndampatsa Aholiabu, mwana wa Ahisama,
wa pfuko la Dani, akhale naye; ndipo ndaika luso m'mitima ya onse a mtima
waluso, kuti apange zonse ndakuuza iwe; 7cihema cokomanako, likasa la
mboni, ndi cotetezerapo ciri pamwamba pace, ndi zipangizo zonse za
cihemaco; 8ndi gomelo ndi zipangizo zace, ndi coikapo nyali coona ndi
zipangizo zace, ndi guwa la nsembe lofukizapo; 9ndi guwa la nsembe
yopsereza ndi zipangizo zace zonse, ndi mkhate ndi tsinde lace; 10ndi zobvala
zotumikira nazo, ndi zobvala zopatulika za Aroni wansembe, ndi zobvala za ana
ace, zakucita nazo nchito ya nsembe; 11ndi mafuta odzoza, ndi cofukiza ca
zonunkhira zokoma za malo opatulika; azicita monga mwa zonse ndakuuza iwe.

Masungidwe a dzuwa la Sabata

12Ndipo Yehova ananena ndi Mose, ndi kuti, 13Koma iwe, lankhula ndi ana a
Israyeli, ndi kuti, Muzisunga masabata anga ndithu; pakuti ndiwo cizindikilo
pakati pa Ine ndi inu mwa mibadwo yanu; kuti mudziwe kuti Ine ndine Yehova
wakukupatulani. 14Ndipo muzisunga Sabata; popeza ndilo lopatulika la kwa
inu; ali yense wakuliipsa aphedwe ndithu; pakuti ali yense wakugwira nchito
m'mwemo, munthu ameneyo asadzidwe mwa anthu a mtundu wace. 15Agwire
nchito masiku asanu ndi limodzi; koma lacisanu ndi ciwiri ndilo Sabata
lakupumula, lopatulika la Yehova; ali yense wogwira nchito tsiku la Sabata
aphedwe ndithu. 16Cifukwa cace ana a Israyeli azisunga Sabata, kucita Sabata
mwa mibadwo yao, likhale pangano losatha; 17ndico cizindikilo cosatha pakati
pa Ine ndi ana a Israyeli; pakuti Yehova analenga zam'mwamba ndi dziko
lapansi masiku asanu ndi limodzi, napumula tsiku lacisanu ndi ciwiri, naonanso
mphamvu.
18Ndipo atatha iye kulankhula ndi Mose, pa phiri la Sinai, anampatsa magome
awiri a mboni, magome amiyala, olembedwa ndi cala ca Mulungu.

Eksodo 32

Fano la mwana wa ng'ombe

1Koma pamene anaona kuti Mose anacedwa kutsika m'phiri, anthuwo anasonkhana kwa Aroni, nanena naye, Ukani, tipangireni milungu yakutitsogolera; pakuti Mose uyu, munthuyu anatikweza kucokera m'dziko la Aigupto, sitidziwa comwe camgwera. 2Ndipo Aroni ananena nao, Thyolani mphete zagolidi ziri; m'makutu a akazi anu, a ana anu amuna ndi akazi, ndi kubwera nazo kwa ine. 3Ndipo anthu onse anathyola mphete zagolidi zinali m'makutu mwao, nabwera nazo kwa Aroni. 4Ndipo anazilandira ku manja ao, nacikonza ndi cozokotera, naciyenga mwana wa ng'ombe; ndipo anati, Siyi milungu yako, Israyeli, imene inakukweza kucokera m'dziko la Aigupto. 5Pakuciona Aroni, anamanga guwa la nsembe patsogolo pace; ndipo Aroni anapfuula nati, Mawa aliko madyerero a Yehova. 6Ndipo m'mawa mwace anauka mamawa, nafukiza nsembe zopsereza, nabwera nazo nsembe zamtendere; ndi anthu anakhala pansi kudya ndi kumwa, nauka kusewera. 7Ndipo Yehova anati kwa Mose, Muka, tsikatu, pakuti anthu ako udakwera nao kucokera m'dziko la Aigupto wadziipsa; 8wapatuka msanga njira imene ndinawauza; wadzinyengera mwana wa ng'ombe, namgwadira, namphera nsembe, nati, Siyi milungu yako, Israyeli, imene inakukweza kucokera m'dziko la Aigupto, 9Ndipo Yehova anati kwa Mose, Ndawapenya anthu awa, taona, ndiwo anthu opulupudza; 10ndipo tsopano ndileke, kuti ndipse mtima pa awo ndi kuwatha, ndi kukuza iwe ukhale mtundu waukuru. 11Ndipo Mose anapemba kwa Yehova Mulungu wace, nati, Yehova, mtima wanu upserenji pa anthu anu, amene munawaturutsa m'dziko la Aigupto ndi mphamvu yaikuru, ndi dzanja lolimba? 12Akaneneranji Aaigupto; ndi kuti, Anawaturutsa coipa, kuti awaphe m'mapiri, ndi kuwatha pankhope pa dziko lapansi? Pepani, lekani coipaco ca pa anthu anu. 13Kumbukilani Abrahamu, Isake ndi Israyeli, atumiki anu, amene munawalumbirira ndi kudzichula nokha, amene munanena nao, Ndidzacurukitsa mbeu zanu ngati nyenyezi za kuthambo, ndi dziko ili lonse ndanenali ndidzapatsa mbeu zanu, likhale colowa cao nthawi zonse. 14Ndipo Yehova analeka coipa adanenaci, kuwacitira anthu ace.

Mose atsikira anthu opembedza fanolo

15Ndipo Mose anatembenuka, natsika m'phirimo, magome awiri a mboni ali m'dzanja lace; magome olembedwa kwina ndi kwina; analembedwa mbali yina ndi inzace yomwe. 16Ndipo magomewo ndiwo nchito ya Mulungu, kulembaku ndiko kulemba kwa Mulungu, kozokoteka pa magomewo. 17Ndipo pamene Yoswa anamva phokoso la kupfuula kwa anthu, anati kwa Mose, Kuli phokoso la nkhondo kucigono. 18Koma iye anati, Phokosoli sindilo la kupfuula kwa olakika, kapena la kupfuula kwa opasuka; koma phokoso ndikumvali ndilo la othirirana mang'ombe. 19Ndipo kunali, pamene anayandikiza cigono, anaona mwana wa ng'ombeyo ndi kubvinako; ndipo Mose anapsa mtima, nataya magome ali m'manja mwace, nawaswa m'tsinde mwa phiri. 20Ndipo anatenga mwana wa ng'ombe anampangayo, namtentha ndi moto, nampera asalale, namwaza pamadzi, namwetsako ana a Israyeli. 21Ndipo Mose anati kwa Aroni, Anthu awa anakucitiranji, kuti iwe watengera iwo kulakwa kwakukuru kotere? 22Ndipo Aroni anati, Asapse mtima mbuye wanga; udziwa anthuwa kuti akhumba coipa. 23Pakuti ananena nane, Tipangireni milungu yakutitsogolera;

popeza Mose uyu, munthuyu anatikweza kucokera m'dziko la Aigupto, sitidziwa comwe camgwera. 24Ndipo ndinanena nao, Ali yense ali naye golidi amthyole; ndipo anandipatsa; ndipo ndinaciponya m'moto, ndimo anaturukamo mwana wa ng'ombe uyu.

Alangidwa anthuwo

25Ndipo pamene Mose anaona kuti anthu anamasuka, popeza Aroni adawamasula kuti awatonze adani ao, 26Mose anaima pa cipata ca cigono, nati, Onse akubvomereza Yehova, adze kwa ine. Pamenepo ana amuna onse a Levi anasonkhana kwa iye, 27Ndipo ananena nao, Atero Yehova Mulungu wa Israyeli, Yense amange lupanga lace m'cuuno mwace, napite, nabwerere kuyambira cipata kufikira cipata, pakati pa cigono, naphe yense mbale wace, ndi yense bwenzi lace, ndi yense mnansi wace. 28Ndipo ana a Levi anacita monga mwa mau a Mose; ndipo adagwa tsiku lija anthu ngati zikwi zitatu. 29Popeza Mose adati, Mdzazireni Yehova manja anu lero, pakuti yense akhale mdani wa mwana wace wamwamuna, ndi mdani wa mbale wace; kuti akudalitseni lero lino.

Mose atetezera anthu kwa Mulungu

30Ndipo kunali m'mawa mwace, kuti Mose anati kwa anthu, Mwacimwa kucimwa kwakukulu; koma ndikwera kwa Yehova tsopano, kapena ndidzacita cotetezera ucimo wanu. 31Ndipo Mose anabwerera kumka kwa Yehova, nati, Ha! pepani, anthu awa anacimwa kucimwa kwakukuru, nadzipangira milungu yagolidi. 32Koma tsopano, kapena mudzakhululukira kucimwa kwao; koma ngati mukana, mundifafanizetu, kundicotsa m'buku lanu limene munalembera, 33Ndipo Yehova anati kwa Mose, iye amene wandicimwira, ndifafaniza yemweyo kumcotsa m'buku langa. 34Ndipo tsopano, muka, tsogolera anthu kumka nao kumene ndinakuuza; taona, mthenga wanga akutsogolera; koma tsiku lakuwazonda Ine ndidzawalanga cifukwa ca kucimwa kwao. 35Ndipo Yehova anakantha anthu, cifukwa anapanga mwana wa ng'ombe amene Aroni anapanga.

Eksodo 33

Mulungu akuti sadzawaperekezanso

1Ndipo Yehova anati kwa Mose, Muka, kwera kucokera kuno, iwe ndi anthu amene unawakweza kucokera m'dziko la Aigupto, kumka ku dzikolo ndinalumbirira nalo Abrahamu, ndi Isake, ndi Yakobo, ndi kuti, Ndidzapatsa mbeu zako ilo; 2ndipo ndidzatuma mthenga akutsogolere; ndipo ndidzapitikitsa Akanani, ndi Aamori, ndi Ahiti, ndi Aperizi, Ahivi, ndi Ayebusi; 3kudziko koyenda mkaka ndi uci ngati madzi; pakuti sindidzakwera pakati pa inu; popeza inu ndinu anthu opulupudza; ndingathe inu panjira. 4Ndipo pamene anthu anamva mau awa oipa anacita cisoni; ndipo panalibe mmodzi anabvala zokometsera zace. 5Ndipo Yehova anati kwa Mose, Nena ndi ana a Israyeli, Inu ndinu anthu opulupudza; ndikakwera kulowa pakati pa inu kamphindi kamadzi, ndidzakuthani; koma tsopano, bvulani zokometsera zanu, kuti ndidziwe comwe ndikucitireni. 6Ndipo ana a Israyeli anazicotsera zokometsera zao kuyambira pa phiri la Horebe.

7Ndipo Mose akatenga cihemaco nacimanga kunja kwa cigono, kutari kwa cigono; nacicha, Cihema cokomanako. Ndipo kunakhala kuti yense wakufuna Yehova anaturuka kumka ku cihema cokomanako kunja kwa cigono. 8Ndipo kunali, pakuturuka Mose kumka ku cihemaco kuti anthu onse anaimirira, nakhala ciriri, munthu yense pakhomo pa hema wace, nacita cidwi pa Mose, kufikira atalowa m'cihemaco. 9Ndipo kunali, pakulowa Mose m'cihemaco, mtambo njo udafutsika, nuima pakhomo pa cihemaco; ndipo Yehova analankhula ndi Mose. 10Ndipo anthu onse anaona mtambo njo ulikuima pakhomo pa cihema; ndi anthu onse anaimirira, nalambira, yense pakhomo pa hema wace. 11Ndipo Yehova ananena ndi Mose kopenyana maso, monga munthu alankhula ndi bwenzi lace. Ndipo anabwerera kumka kucigono; koma mtumiki wace Yoswa, mwana wa Nuni, ndiye mnyamata msinkhu wace, sanacoka m'cihemamo.

Mose apeza ufulu pamaso pa Mulunsu

12Ndipo Mose anati kwa Yehova, Taonani, Inu munena ndi ine, Kwera nao anthu awa; koma simunandidziwitsa amene mudzamtuma amuke nane. Koma munati, Ndikudziwa dzina lako, wapezanso ufulu pamaso panga, 13Ndipo tsopano, ngati ndapeza ufulu pamaso panu, mundidziwitsetu njira zanu, kuti ndikudziweni, ndi kuti ndipeze ufulu pamaso panu; ndipo penyani kuti mtundu uwu ndi anthu anu. 14Ndipo anati, Nkhope yanga idzamuka nawe, ndipo ndidzakupumuza. 15Ndipo ananena ndi Iye, Ikapanda kumuka nane nkhope yanu, musatikweze kucokera kuno. 16Pakuti cidziwfka ndi ciani tsopano kuti ndapeza ufulu pamaso panu, ine ndi anthu anu? Si pakumuka nafe Inu, kuti ine ndi anthu anu tisiyane ndi anthu onse akukhala pa nkhope ya dziko lapansi? 17Ndipo Yehova anati kwa Mose, Ici comwe wanenaci ndidzacita; pakuti wapeza ufulu pamaso panga, ndipo ndikudziwa dzina lako. 18Ndipo anati, Ndionetsenitu ulemerero wanu. 19Ndipo iye anati, Ndidzapititsa ukoma wanga wonse pamaso pako, ndipo ndidzachula dzina la Yehova pamaso pako; ndipo ndidzacitira ufulu amene ndidzamcitira ufulu; ndi kucitira cifundo amene ndidzamcitira cifundo. 20Ananenanso, Sungathe kuona nkhope yanga; pakuti palibe munthu adzandiona Ine ndi kukhala ndi moyo. 21Ndipo Yehova anati, Taona pali Inepo pali malo, ndipo uime pathanthwe; 22ndipo kudzakhala,

pakupitira olemerero wanga, ndidzakuika mu mpata wa thanthwe, ndi kukuphimba ndi dzanja langa, mpaka nditapitira; 23ndipo pamene ndicotsa dzanja langa udzaona m'mbuyo mwanga; koma nkhope yanga siidzaoneka.

Eksodo 34

Magome atsopano a Malamulowo

1Ndipo Yehova anati kwa Mose, Dzisemere magome awiri amiyala onga
oyamba aja; ndipo ndidzalembera pa magomewo mau omwewo anali pa
magome oyambawo, amene unawaswa. 2Nukonzekeretu m'mawa, nukwere
m'mawa m'phiri la Sinai, nuimepo pamaso panga pamwamba pa phiri. 3Palibe
munthu akwere ndi iwe, asaonekenso munthu ali yense m'phiri monse; ndi
zoweta zazing'ono kapena zoweta zazikuru zisadye kuphiri kuno. 4Ndipo
anasema magome awiri a miyala, onga oyamba aja; ndipo Mose anauka
mamawa nakwera m'phiri la Sinai, monga Yehova adamuuza, nagwira m'dzanja
mwace magome awiri amiyala. 5Ndipo Yehova anatsika mumtambo, naimapo
pamodzi ndi iye, napfuula dzina la Yehova. 6Ndipo Yehova anapita pamaso
pace, napfuula, Yehova, Yehova, Mulungu wacifundo ndi wacisomo,
wolekereza, ndi wa ukoma mtima wocuruka, ndi wacoonadi; 7wakusungira
anthu osawerengeka cifundo, wakukhululukira mphulupulu ndi kulakwa ndi
kucimwa; koma wosamasula woparamula; wakulangira ana ndi zidzukulu
cifukwa ca mphulupulu ya atate ao, kufikira mbadwo wacitatu ndi
wacinai. 8Ndipo Mose anafulumira, naweramira pansi, nalambira. 9Ndipo anati,
Ngati ndapeza ufulu tsopane pamaso panu, Ambuye, ayendetu Ambuye pakati
pa ife; pakuti awa ndi anthu opulupudza; ndipo mutikhululukire mphulupulu ndi
ucimo wathu, ndipo mutilandire tikhale colowa canu. 10Ndipo iye anati, Taona,
Ine ndicita pangano; ndidzacita zozizwa pamaso pa anthu ako onse, sizinacitika
zotere ku dziko lonse lapansi, kapena ku mtundu uti wonse wa anthu; ndipo
anthu onse amene uli pakati pao adzaona nchito ya Yehova, pakuti cinthu
ndikucitiraci ncoopsa. 11Dzisungire cimene Ine ndikuuza lero lino: taona,
ndiingitsa pamaso pako Aamori ndi Akanani, ndi Ahiti ndi Aperizi, ndi Ahivi, ndi
Ayebusi. 12Dzicenjere ungacite pangano ndi anthu a ku dziko limene umukako,
lingakhale msampha pakati panu; 13koma mupasule maguwa a nsembe ao, ndi
kuphwanya zoimiritsa zao, ndi kulikha zifanizo zao; 14pakuti musalambira
mulungu wina; popeza Yehova dzina lace ndiye Wansanje, ali Mulungu
wansanje; 15ungacite pangano ndi iwo okhala m'dzikomo; ndipo angacite
cigololo pakutsata milungu yao, nangaphere nsembe milungu yao, ndipo
angakuitane wina, nukadye naye nsembe zace; 16ndipo ungatengereko ana
ako amuna ana ao akazi; nangacite cigololo ana ao akazi potsata milungu yao,
ndi kucititsa ana anu amuna cigololo potsata milungu yao. 17Usadzipangire
milungu yoyenga. 18Uzisunga madyerero a mkate wopanda cotupitsa. Uzidya
mkate wopanda cotupitsa masiku asanu ndi awiri, monga ndakuuza pa nthawi
yonenedwa, m'mwezi wa Abibu; pakuti mwezi wa Abibu unaturuka
m'Aigupto. 19Onse oyambira kubadwa ndi anga; ndi zoweta zanu zonse
zazimuna, zoyamba za ng'ombe ndi za nkhosa. 20Koma woyamba wa buru
uzimuombola ndi mwana wa nkhosa; ukapanda kumuombola, uzimthyola khosi.
Ana anu amuna oyamba onse uziwaombola. Ndipo asamaoneka pamaso
panga opanda kanthu. 21Masiku asanu ndi limodzi uzigwira nchito, koma
lacisanu ndi ciwiri uzipumula; nyengo yakulima ndi nyengo yamasika
uzipumula. 22Ndipo uzicita madyerero a masabata, ndiwo madyerero a zipatso
zoyamba za masika a tirigu, ndi madyerero a kututa pakutha pa caka. 23Amuna
ako onse azioneka pamaso pa Yehova Mulungu, Mulungu wa Israyeli, katatu

caka cimodzi. 24Pakuti ndidzaingitsa mitundu ya anthu pamaso pako, ndi
kukulitsa malire ako; ndipo palibe munthu adzakhumba dziko lako, pakukwera
iwe kudzaoneka pamaso pa Yehova Mulungu wako katatu caka
cimodzi. 25Usapereke mwazi wa nsembe yanga yophera pamodzi ndi mkate
wacotupitsa; ndi nsembe yophera ya madyerero a Paskha asaisiye kufikira
m'mawa. 26Uzibwera nazo zipatso zoyambayamba za nthaka yako ku nyumba
ya Yehova Mulungu wako. Usaphika mwana wa mbuzi mu mkaka wa
mace. 27Ndipo Yehova anati kwa Mose, Ulembere mau awa; pakuti monga
mwa mau awa ndapangana ndi iwe ndi Israyeli. 28Ndipo anakhala pomwepo
ndi Yehova masiku makumi anai, usana ndi usiku; sanadya mkate kapena
kumwa madzi. Ndipo analembera pa magomewo mau a panganolo, mau
khumiwo.

Nkhope ya Mose inyezimira

29Ndipo kunali pakutsika Mose pa phiri la Sinai, ndi magome awiri a mboni
m'dzanja lace la Mose, pakutsika iye m'phirimo, Mose sanadziwa kuti khungu la
nkhope yace linanyezimira popeza iye adalankhula naye. 30Ndipo pamene
Aroni ndi ana onse a Israyeli anaona Mose, taonani, khungu la nkhope yace
linanyezimira; ndipo anaopa kumyandikiza. 31Koma Mose anawaitana; ndipo
Aroni ndi akazembe onse a khamu la anthu anabwera kwa iye; ndipo Mose
analankhula nao. 32Ndipo atatero, ana onse a Israyeli anayandikiza; ndipo iye
anawauza zonse Yehova adalankhula naye m'phiri la Sinai. 33Ndipo Mose
atatha kulankhula nao, anaika cophimba pankhope pace. 34Koma pakulowa
Mose pamaso pa Yehova kunena ndi iye, ariacotsa cophimbaco, kufikira
akaturuka; ndipo ataturuka analankhula ndi ana a Israyeli cimene
adamuuza. 35Ndipo ana a Israyeli anaona nkhope ya Mose, kuti khungu la
nkhope ya Mose linanyezimira; ndipo Mose anaikanso cophimba pankhope
pace, kufikira akalowa kulankhula ndi iye.

Eksodo 35

Zopereka zofunika za pa cihemaco

1Ndipo Mose anasonkhanitsa khamu lonse la ana a Israyeli, nanena nao, Siwa
mau amene Yehova anauza, kuti muwacite. 2Masiku asanu ndi limodzi azigwira
nchito; koma tsiku lacisanu ndi ciwiri muliyese lopatulika, Sabata lakupuma la
Yehova: ali yense agwira nchito pamenepo, aphedwe, 3Musamasonkha mota
m'nyumba zanu ziri zonse tsiku la Sabata.
4Ndipo Mose ananena ndi khamu lonse la ana a Israyeli, ndi kuti, Ici ndi cimene
Yehova anauza ndi kuti, 5Mumtengere Yehova copereka ca mwa zanu; ali
yense wa mtima womfunitsa mwini abwere naco, ndico copereka ca
Yehova; 6golidi, ndi siliva, ndi mkuwa; ndi lamadzi, ndi lofiirira, ndi lofiira, ndi
bafuta wa thonje losansitsa, ndi ubweya wa mbuzi; 7ndi zikopa za nkhosa
zamphongo zonika zofiira, ndi zikopa za akatumbu, ndi mtengo wasitimu; 8ndi
mafuta akuunikira, ndi zonunkhira za mafuta odzoza, ndi cofukiza ca pfungo
lokoma; 9ndi miyala yasohamu, ndi miyala yoika ya efodi, ndi ya
capacifuwa. 10Ndipo abwere yense wa mtima waluso mwa inu, napange zonse
zimene Yehova anauza; 11kacisi, hema wace, ndi cophimba cace, zokowera
zace, ndi matabwa ace, mitanda yace, mizati, nsanamira, ndi nsici zace, ndi
makamwa ao; 12likasa, ndi mphiko zace, cotetezerapo, ndi nsaru yocinga
yotseka; 13gome, ndi mphiko zace, ndi zipangizo zace zonse, ndi mkate
woonekera; 14ndi coikapo nyali ca kuunika, ndi zipangizo zace, ndi nyali zace,
ndi mafuta a kuunika; 15ndi guwa la nsembe lofukizapo, ndi mphiko zace, ndi
mafuta odzoza, ndi cofukiza ca pfungo lokoma, ndi nsaru yotsekera pakhomo,
pa khomo la kacisi; 16guwa la nsembe yopereza, ndi made amkuwa, mphiko
zace, ndi zipangizo zace zonse, mkhate ndi tsinde lace; 17nsaru zocingira za
kubwalo, nsici zace, ndi makamwa ace, ndi nsaru yotsekera ku cipata ca
pabwalo; 18ziciri za cihema, ndi ziciri za kubwalo, ndi zingwe zao; 19zobvala za
kutumikira nazo m'maopatulika, zobvala zopatulika za. Aroni wansembe, ndi
zobvala za ana ace, zakugwira nazo nchito ya nsembe.

Anthu abwera ndi zopereka mwaufulu

20Ndipo khamu lonse la ana a Israyeli linacoka pamaso pa Mose. 21Ndipo
anadza, ali yense wofulumidwa mtima, ndi yense mzimu wace wamfunitsa,
nabwera naco copereka ca Yehova, ca ku nchito ya cihema cokomanako, ndi
ku utumiki wace wonse, ndi ku zobvala zopatulika. 22Ndipo anadza amuna ndi
akazi, onse akufuna mtima eni ace, nabwera nazo mphete za mphuno, mphete
za m'makutu, ndi mphete zosindikizira, ndi zidzingwiri, zonsezi zokometsera
zagolidi; inde yense wakupereka kwa Yehova copereka cagolidi. 23Ndipo ali
yense kwao kunapezeka lamadzi, ndi lofiirira, ndi lofiira, ndi bafuta wa thonje
losansitsa, ndi ubweya wa mbuzi, ndi zikopa za nkhosa zamphongo zonika
zofiira, ndi zikopa za akatumbu, anabwera nazo. 24Yense wakupereka
copereka ca siliva ndi mkuwa, anabwera naco copereka ca Yehova; ndi yense
amene kwao kunapezeka mtengo wasitimu wa ku macitidwe onse a nchitoyi,
anabwera nao. 25Ndi akazi onse a mtima waluso anapota ndi manja ao,
nabwera nalo thonje lamadzi, ndi lofiirira, ndi lofiira, ndi bafuta wa thonje
losansitsa. 26Ndi akazi onse ofulumidwa mtima ndi luso anapota ubweyawo wa
mbuzi. 27Ndi akuru anabwera nayo miyala yasohamu, ndi miyala yoti aiike
kuefodi, ndi kucapacifuwa; 28ndi zonunkhira, ndi mafuta akuunikira, ndi mafuta

odzoza, ndi cofukiza za pfungo lokoma. 29Amuna ndi akazi onse a ana a Israyeli amene mitima yao inawafunitsa eni kubwera nazo za ku nchito yonse imene Yehova anauza Ipangike ndi dzanja la Mose, anabwera naco copereka cofuna mwini, kucipereka kwa Yehova.
30Ndipo Mose anati kwa ana a Israyeli, Taonani, Yehova anaitana, ndi kumchula dzina lace, Bezaleli, mwana wa Uri, mwana wa Huri, wa pfuko la Yuda; 31ndipo anamdzaza ndi mzimu wa Mulungu, ndi luso, ndi nzeru, ndi cidziwitso, za m'nchito ziri zonse; 32kulingirira nchito zaluso, kucita ndi golidi, ndi siliva, ndi mkuwa; 33ndi kuzokota miyala voikika, ndi kuzokota mitengo, kucita m'nchito ziri zonse zaluso. 34Ndipo anaika m'mtima mwace kuti alangize ena, iye ndi Aholiabu mwana wa Ahisama, wa pfuko la Dani. 35Amenewo anawadzaza ndi luso lamtima, lakucita nchito ziri zonse, ya kuzokota miyala, ndi ya mmisiri waluso, ndi ya wopikula ndi lamadzi ndi lofiirira, ndi lofiira, ndi bafuta wa thonje losansitsa, ndi ya muomba, ya iwo akucita nchito iri yonse, ndi ya iwo olingirira nchito yaluso.

Eksodo 36

Pamenepo anacita Bezaleli ndi

1Aholiabu, ndi anthu aluso, amene Yehova adaika luso ndi nzeru m'mtima
mwao adziwe macitidwe ace a nchito yonse ya utumiki wace wa malo opatulika,
monga mwa zonse adauza Yehova.

Amisiri alandira zopereka za anthu

2Ndipo Mose adaitana Bezaleli ndi Aholiabu, ndi anthu onse aluso, amene
Yehova adaika luso m'mtima mwao, onse ofulumidwa mtima ayandikize
kunchito kuicita. 3Ndipo analandira kwa Mose copereka conse, cimene ana a
Israyeli adabwera naco cikhale ca macitidwe a nchito ya malo opatulika,
aipange naco. Koma anaonjeza kubwera nazo kwa iye zopereka zofuna mwini,
m'mawa ndi m'mawa. 4Ndipo aluso onse, akucita nchito yonse ya malo
opatulika, anadza onse ndi kusiya nchito yao: analinkucita; 5nanena ndi Mose,
ndi kuti, Anthu alinkubwera nazo zocuruka, zakuposera zoyenera nchito imene
Yehova anauza icitike. 6Ndipo Mose analamulira, ndipo anamveketsa mau mwa
cigono conse, ndi kuti, Asaonjezere nchito ya ku copereka ca malo opatulika,
ngakhale mwamuna ngakhale mkazi. Tero anawaletsa anthu asabwere nazo
zina. 7Popeza zipangizo zinakwanira nchito yonse icitike, zinatsalakonso.

Mapangidwe a cihemaco

8Ndipo onse a mtima waluso mwa iwo akucita nchitoyi anapanga kacisi ndi
nsaru zophimba khumi; anaziomba ndi bafuta wa thonje losansitsa, ndi lamadzi;
ndi lofiira, ndi lofiira, ndi akerubi, nchito ya mmisiri. 9Utali wace wa nsaru
yophimba imodzi ndiwo mikono makumi awiri kudza isanu ndi itatu, ndi
kupingasa kwace kwa nsaru imodzi mikono inai; nsaru zonse zinafanana
muyeso wao. 10Ndipo analumikiza nsaru zisanu yina ndi inzace; nalumikiza
nsaru zisanu zina yina ndi inzace. 11Ndipo anaika magango ansaru yamadzi
m'mphepete mwace mwa nsaru imodzi ku mkawo wa cilumikizano; nacita
momwemo m'mphepete mwace mwa nsaru ya kuthungo, ya cilumikizano
caciwiri. 12Anaika magango makumi asanu pa nsaru imodzi, naikanso
magango makumi asanu m'mphepete mwace mwa nsaru ya cilumikizano cina;
magango anakomanizana lina ndi linzace. 13Ndipo anazipanga zokowera
makumi asanu zagolidi, namanga nsaru pamodzi ndi zokowerazo; ndipo kacisi
anakhala mmodzi. 14Ndipo anaomba nsaru zophimba za ubweya wa mbuzi
zikhale hema pamwamba pa kacisi; anaomba nsaru zophimba khumi ndi
imodzi. 15Utali wace wa nsaru imodzi ndiwo mikono makumi atatu, ndi
kupingasa kwace kwa nsaru imodzi ndiko mikono inai; nsaru khumi ndi imodzi
zinafanana muyeso wao. 16Ndipo anamanga pamodzi nsaru zisanu pa zokha,
ndi nsaru zisanu ndi imodzi pa zokha. 17Ndipo anapanga magango makumi
asanu m'mphepete mwa nsaru imodzi, ya kuthungo, ya cilumikizano, naika
magango makumi asanu m'mphepete mwa nsaru ya kuthungo, ya cilumikizano
cina. 18Ndipo anapanga zokowera makumi asanu zamkuwa kumanga pamodzi
hemalo, kuti likhale limodzi. 19Ndipo anasokera hemalo cophimba ca zikopa za
nkhosa zamphongo zonika zofiira, ndi cophimba ca zikopa za akatumbu
pamwamba pace.

20Ndipo anapanga matabwa a kacisi, oimirika, a mtengo wasitimu. 21Utali
wace wa thabwa limodzi ndiwo mikono khumi, ndi kupingasa kwace kwa
thabwa limodzi ndiko mkono ndi hafu. 22Pa thabwa limodzi panakhala

mitsukwa iwiri, yomangika pamodzi; anawapanga momwemo matabwa onse a kacisi. 23Ndipo anapanga matabwa a kacisi; matabwa makumi awiri a ku mbali ya kumwela, kumwela; 24napanga makamwa makumi anai pansi pamatabwa makumi awiri; makamwa awiri pansi pa thabwa limodzi kwa mitsukwa yace iwiri, ndi makamwa awiri pansi pa thabwa lina kwa mitsukwa yace iwiri. 25Ndi ku mbali yina ya kacisi, mbali ya kumpoto, anapanga matabwa makumi awiri, ndi makamwa ao makumi anai asiliva; 26makamwa awiri pansi pa thabwa limodzi, ndi makamwa awiri pansi pa thabwa lina. 27Ndi ku mbali ya kumbuyo ya kacisi kumadzulo anapanga matabwa asanu ndi limodzi. 28Anapanganso matabwa awiri a ku ngondya za kacisi, m'mbali zace ziwirio 29Ndipo anaphatikizika pamodzi patsinde, naphatikizilca pamodzi pamutu pace ndi mphete imodzi; anatero nao onse awiri pa ngondya ziwiri. 30Ndipo panali matabwa asanu ndi atatu ndi makamwa ao asiliva, makamwa khumi kudza asanu ndi limodzi; makamwa awiri pansi pa thabwa limodzi. 31Ndipo anapanga mitanda ya mtengo wasmmu; Isanu ya matabwa a pa mbali yina ya kacisi, 32ndi mitanda isanu ya matabwa a pa mbali inzace ya kacisi, ndi mitanda lsanu ya matabwa a kacisi ali pa mbali ya kumadzulo. 33Ndipo anapititsa mtanda wa pakatipo, pakati pa matabwa kufikira kuthungo. 34Ndipo anakuta matabwa ndi golidi, napanga mphete zao zagolidi zikhale zopisamo mitandayo, nakuta mitandayo ndi golidi.
35Ndipo anaomba nsaru yocinga ndi lamadzi, ndi lofiirira, ndi lofiira, ndi bafuta wa thonje losansitsa; anaciomba ndi akerubi nchito ya mmisiri. 36Ndipo anaipangira mizati inai yasitimu, nazikuta ndi golidi; zokowera zao zinali zagolidi; ndipo anaziyengera makamwa anai asiliva. 37Ndipo anaomba nsaru yotsekera pa khomo la cihemaco, ya lamadzi, ndi lofiirira, ndi lofiira, ndi bafuta wa thonje losansitsa, nchito ya wopikula; 38ndi nsamamira zace zisanu ndi zokowera zao; nakuta mitu yao ndi mitanda yao ndi golidi; ndi makamwa ao asanu anali amkuwa.

Eksodo 37

Mapangidwe a likasa

1Ndipo Bezaleli anapanga likasa la mtengo wasitimu; utali wace mikono iwiri ndi hafu, ndi kupingasa kwace mkono ndi hafu, ndi msinkhu wace mkono ndi hafu; 2ndipo analikuta ndi golidi woona m'kati ndi kunja, nalipangira mkombero wagolidi pozungulira pace. 3Ndipo analiyengera mphete zinai zagolidi pa miyendo yace inai; mphete ziwiri pa mbali yace imodzi, ndi mphete: ziwiri pa mbali yace yina. 4Ndipo anapanga mphiko za mtengo wasitimu, nazikuta ndi golidi. 5Ndipo anapisa mphiko m'mphetezo pa mbali zace za likasalo, kuti anyamulire nazo likasa. 6Ndipo anapanga cotetezerapo ca golidi woona; utali wace mikono iwiri ndi hafu, ndi kupingasa kwace mkono ndi hafu. 7Anapanganso akerubi awiri agolidi; anacita kuwasula mapangidwe ace, pa mathungo ace swiri a coteteze rapo; 8kerubi mmodzi pa mbali yace imodzi, ndi kerubi wilia pa mbali yace yina; anapanga akerubi ocokera m'cotetezerapo, pa mathungo ace awiri. 9Ndipo akerubi anafunyulira mapiko ao m'mwamba, ndi kuphimba cotetezerapo ndi mao piko ao, ndi nkhope zao zopeoyana; zinapenya kucotetezerapo nkhope zao.

Gome La mkate woonekera

10Ndipo anapanga gome la mtengo wasitimu; utali wace mikono iwiri, ndi kupingasa kwace mkono limodzi, ndi msinkhu wace mkono ndi hafu; 11ndipo analikuta ndi golidi woona, nalipangira mkombero wagolidi pozungulira pace. 12Analipangiranso mitanda pozungulirapo, yoyesa cikhato m'kupingasa kwace, ndi pamitanda pace pozungulira anapangirapo mkombero wagolidi. 13Ndipo analiyengera mphete zinai zagolidi, naika mphetezo pa ngondya zace zinai zokhala pa miyendo yace inai. 14Mphetezo zinali pafupi pa mitanda, zikhale zopisamo mphiko kunyamulira nazo gomelo. 15Ndipo anapanga mphiko za mtengo wasitimu, nazikuta ndigolidi, kunyamulira nazo gomelo. 16Anapanganso zipangizo za gomelo, mbale zace, ndi zipande zace, ndi mitsuko yace, ndi zikho zace zakuthira nazo, za golidi woona.

Coikapo nyali

17Ndipo anapanga coikapo nyali ca golidi woona; mapangidwe ace a coikapo nyalico anacita cosula, tsinde lace ndi thupi lace, zikho zace, mitu yace, ndi maluwa ace zinakhala zocokera m'mwemo; 18ndi m'mbali zace munaturuka mphanda zisanu ndi imodzi; mphanda zitatu za coikapo nyali zoturuka m'mbali yace imodzi, ndi mphanda zitatu za coikapo nyali zoturuka m'mbali yace yina; 19pa mphanda imodzi panali zikho zitatu zopangika ngati katungurume, mutu ndi luwa; ndi pa mphanda yina zikho zitatu zopangika ngati katungurume, mutu ndi luwa; zinatero mphanda zisanu ndi imodzi zoturuka m'coikapo nyali. 20Ndipo pa coikapo nyali comwe panali zikho zinai zopangika ngati katungurume, mitu yace ndi maluwa ace; 21ndipo panali mutu pansi pa mphanda ziwiri, zoturuka m'mwemo, ndi mutu pansi pa mphanda ziwiri, zoturuka m'mweno, ndi mutu pansi pa mphanda ziwiri, zoturuka m'mwemo, inatero pa mphanda zisanu ndi imodzi zocokera m'mwemo. 22Mitu yao ndi mphanda zao zinaturuka m'mwemo; conseci cinali cosulika pamodzi ca golidi woona. 23Ndipo anapanga nyali zace zisanu ndi ziwiri ndi mbano zace, ndi zoolera zace, za golidi woona. 24Anacipanga ici ndi zipangizo zace zonse za talente wa golidi woona.

Guwa lofukizapo

25Ndipo anapanga guwa la nsembe lofukizapo la mtengo wasitimu; utali wace
mkono, ndi kupingasa kwace mkono, lampwamphwa; ndimsinkhu wace mikono
iwiri; nyanga zace zinaturuka m'mwemo. 26Ndipo analikuta ndi golidi woona,
pamwamba pace, ndi mbali zace pozungulira, ndi nyanga zace; ndipo
analipangira mkombero wagolidi pozungulira pace. 27Ndipo analipangira
mphete ziwiri zagolidi pansi pa mkombero wace, pa ngondya zace ziwiri, pa
mbali zace ziwiri, zikhale zopisamo mphiko kulinyamulira nazo. 28Ndipo
anazipanga mphiko za mtengo wasitimu, nazikuta ndi golidi. 29Anapanganso
mafuta opatulika akudzoza nao, ndi cofukiza coona ca pfungo lokoma, mwa
macitidwe a wosanganiza.

Eksodo 38

Mapangidwe a guwa la nsembe yopsereza

1Ndipo anapanga guwa la nsembe yopsereza la mtengo wasitimu; utali wace
mikono isanu, ndi kupingasa kwace mikono isanu, lampwamphwa; ndi msinkhu
wace mikono itaru. 2Ndipo anapanga nyanga zace pa ngondya zace zinai;
nyanga zace zinakhala zoturuka m'mwemo; ndipo analikuta ndi
mkuwa. 3Anapanganso zipangizo zonse za guwalo, zotayira, ndi zoolera, ndi
mbale zowazira, ndi mitungo, ndi zoparira moto; zipangizo zace zonse
anazipanga zamkuwa. 4Ndipo anapangira guwa La nsembelo made, malukidwe
ace nja mkuwa, pansi pa matso ace wakulekeza pakati pace. 5Ndipo
anayengera mathungo anai a made amkuwawo mphete zinai, zikhale zopisamo
mphiko. 6Napanga mphiko za mtengo wasitimu, nazikuta ndi mkuwa. 7Ndipo
anapisa mphikozo m'zimphetemo pa mbali za guwa la nsembe, kulinyamulira
nazo; analipanga ndi matabwa, lagweregwere.
8Ndipo anapanga mkhate wamkuwa, ndi tsinde lace lamkuwa, wa akalirole a
akazi otumikira, akutumikira pa khomo la cihema cokomanako.

Bwalo La cihema

9Ndipo anapanga bwalo; pa mbali ya kumwela, kumwela, nsaru zocingira za
pabwalo zinali za bafuta wa thonje losansitsa, mikono zana limodzi; 10nsici
zace makumi awiri, ndi makamwa ao makumi awiri, amkuwa; zokowera za nsici
ndi mitanda yace zasiliva. 11Ndi pa mbali ya kumpoto mikono zana limodzi,
nsici zace makumi awiri, nw makamwa ace makumi awiri, amkuwa; zokowera
za nsici ndi mitanda yace yasiliva. 12Ndi pa mbali ya kumadzulo panali nsaru
zocingira za mikono makumi asanu, nsid zace khumi, ndi makamwa ace khumi;
zokowera za nsici ndi mitanda yace yasiliva. 13Ndi pa mbali ya kum'mawa,
kum'mawa, mikono makumi asanu. 14Nsaru zocingira za pa mbali imodzi ya
cipata nza mikono khumi ndi isanu; nsici zace zitatu, ndi makamwa ace
atatu; 15momwemonso pa mbali yina: pa mbali yino ndi pa mbali yina ya cipata
ca pabwalo panali nsaru zocingira za mikono khumi ndi isanu; nsici zace zitatu,
ndi makamwa ace atatu. 16Nsaru zocingira zonse za pabwalo pozungulira
zinali za bafuta wa thonje losansitsa. 17Ndipo makamwa a nsici anali amkuwa;
zokowera za nsici ndi mitanda Iyace zasiliva; ndi zokutira mitu yace zasiliva; ndi
nsici zonse za pabwalo zinagwirana pamodzi ndi siliva. 18Ndi nsaru yotsekera
pa cipata ca pabwalo ndiyo nchito ya wopikula, ya lamadzi, ndi lofiirira, ndi
lofiira, ndi bafuta wa thonje losansitsa; utali wace mikono makumi awiri, ndi
msinkhu wace mu kupingasa kwace mikono isanu, yolingana ndi nsaru
zocingira za pabwalo. 19Ndi nsici zace zinali zinai, ndi makamwa ace anai,
amkuwa; zokowera zace zasiliva, ndi zokutira mitu yace ndi mitanda yace
zasiliva. 20Ndi ziciri zonse za cihema, ndi za bwalo lace pozungulira, nza
mkuwa.

Mawerengo a zopereka za pa cihemao

21Ici ndi ciwerengo ca zinthu za cihema, cihema ca mboni, monga
anaziwerenga, monga mwa mau a Mose, acite nazo Alevi; anaziwerenga
Itamara, mwana wa Aroni wansembe. 22Ndipo Bezaleli mwana wa Uri, mwana
wa Huri, wa pfuko la Yuda, anapanga zonse zimene Mulungu adauza
Mose. 23Ndi pamodzi naye Aholiabu, mwana wa Ahisama, wa pfuko la Dani,

ndiye wozokota miyala, ndi mmisiri waluso, ndiponso wopikula ndi lamadzi ndi lofiira, ndi lofiira, ndi bafuta wa thonje losansitsa.
24Golidi yense anacita naye mu nchito yonse ya malo opatulika, golidi wa coperekaco, ndico matalente makumi awiri kudza asanu ndi anai, ndi masekeli mazana asanu ndi awiri, kudza makumi atatu, monga mwa sekeli wa malo opatulika. 25Ndipo siliva wa iwo owerengedwa a khamulo ndiwo matalente zana limodzi, ndi masekeli cikwi cimodzi, kudza mazana asanu ndi awiri, mphambu makumi asanu ndi awiri kudza asanu, kuyesa sekeli wa malo opatulika; 26munthu mmodzi anapereka beka, ndiwo limodzi la magawo awiri la sekeli, kuyesa sekeli wa malo opatulika, anatero onse akupita kumka kwa owerengedwawo, kuyambira munthu wa zaka makumi awiri ndi oposa, ndiwo anthu zikwi mazana asanu ndi limodzi kudza zitatu, ndi mazana asanu mphambu makumi asanu. 27Ndipo matalente zana limodzi a siliva ndiwo a kuyengera makamwa a malo opatulika, ndi makamwa a nsaru yocinga; makamwa zana limodzi matalente zana limodzi, talente limodzi kamwa limodzi. 28Ndipo anapanga zokowera za mizati nsanamira ndi nsici ndi masekeli aja cikwi cimodzi kudza mazana asanu ndi awiri mphambu asanu, nakuta mitu yace, nazigwirizitsana pamodzi. 29Ndi mkuwa wa coperekaco ndiwo matalente makumi asanu ndi awiri, ndi masekeli zikwi ziwiri kudza mazana anai. 30Ndipo anapanga nao makamwa a pa khomo la cihema cokomanako, ndi guwa la nsembe lamkuwa, ndi made ace amkuwa, ndi zipangizo zonse za guwa la nsembe, 31ndi makamwa a pabwalo pozungulira, ndi makamwa a ku cipata ca pabwalo, ndi ziciri zonse za cihema, ndi ziciri zonse za pabwalo pozungulira.

Eksodo 39

Maombedwe a zobvala za ansembe

1Ndipo anaomba zobvala zakutumikira nazo ndi lamadzi, ndi lofiirira, ndi lofiira, atumikire nazo m'malo opatulika, naomba zobvala zopatulika za Aroni; monga Yehova adamuuza Mose.

2Ndipo anaomba efodi wa golidi, lamadzi, lofiirira, ndi lofiira, ndi bafuta wa thonje losansitsa. 3Ndipo anasula golidi waphanthiphanthi, nalemba nsambo, kuti amuombe pamodzi ndi lamadzi, ndi lofiirira, ndi lofiira, ndi bafuta wa thonje losansitsa, nchito ya mmisiri. 4Anapangira efodi zapamapewa zolumikizana; pa nsonga ziwirizo anamlumikiza. 5Ndi mpango wa efodi wokhala pamenepo, wakummanga nao unali woombera kumodzi wa ciombedwe comweci; wa golidi, ndi lamadzi, ndi lofiirira, ndi lofiira, ndi bafuta wa thonje losansitsa; monga Yehova adauza Mose.

6Ndipo anakonza miyala yasohamu, yogwirika m'zoikamo zagolidi, yoloca ngati malocedwe a cosindikizira, ndi maina a ana a lsrayeli. 7Ndipo anaiika pa zapamapewa za efodi, ikhale miyala ya cikumbutso kwa ana a Israyeli; monga Yehova adamuuza Mose.

8Ndipo anaomba capacifuwa, nchito ya mmisiri, monga maombedwe ace a efodi; ca golidi, lamadzi, ndi lofiirira, ndi lofiira, ndi bafuta wa thonje losansitsa. 9Cinakhala camowamphwa; anaciomba capacifuwa copindika; utali wace cikhato cimodzi, ndi kupingasa kwace cikhato cimodzi, cinakhala copindika. 10Ndipo anaika pomwepo mizere inai ya miyala; mzere wa odemu, pitida, ndi bareketi, ndiyo ya mzere woyamba. 11Ndi mzere waciwiri wa nofeki, safiri, ndi yahalomu. 12Ndi mzere wacitatu wa lesemu, sibu, ndi akalama. 13Ndi mzere wacinai wa tarisisi, sohamu, ndi yasefe; inakhala yogwirika ndi golidi maikidwe ace. 14Ndipo miyalayi inakhala monga mwa maina a ana a Israyeli, khumi ndi awiri, monga mwa maina ao; ngati malocedwe a cosindikizira, yonse monga mwa maina ace, kwa mafuko khumi ndi awiriwo. 15Ndipo anapangira pacapacifuwa maunyolo ngati zingwe, nchito yopota ya golidi woona. 16Anapanganso zoikamo ziwiri zagolidi, ndi mphete ziwiri zagolidi; naika mphete ziwirizo pa nsonga ziwiri za capacifuwa. 17Ndipo anamanga maunyolo awiri opota agolidi pa mphete ziwiri pa nsonga za capacifuwa. 18Ndi nsonga zace ziwiri zina za maunyolo awiri opotawo anazimanga pa zoikamo ziwiri, nazimanga pa zapamapewa za efodi, m'tsogolo mwace. 19Ndipo anapanga mphete ziwiri zagolidi, naziika pa nsonga ziwiri za capacifuwa, m'mphepete mwace m'katimo, pa mbali ya kuefodi. 20Ndipo anapanga mphete ziwiri zagolidi, naziika pa zapamapewa ziwiri za efodi pansi pace, pa mbali yace ya kutsogolo, pafupi pa msoko wace, pamwamba pa mpango wa efodi. 21Ndipo anamanga capacifuwa pa mphete zace ndi mphete za efodi ndi mkuzi wamadzi, kuti cikhale pa mpango wa efodi, ndi kuti capacifuwa cisamasuke paefodi; monga Yehova anamuuza Mose.

22Ndipo anaomba mwinjiro wa efodi, nchito yoomba ya lamadzi lokha; 23ndi pakati pace polowa mutu, ngati polowa pa maraya ocingirizira, ndipo anabinyira pozungulira polowa pace, pangang'ambike. 24Napangira pa mkawo wa mwinjiro makangaza a lamadzi, ndi lofiirira, ndi lofiira, ndi bafuta wa thonje losansitsa. 25Ndipo anapanga miriu ya golidi woona, napakiza miriu ndi makangaza, pa mkawo wa mwinjiro pozungulira, popakiza ndi

makangaza. 26Mliu ndi khangaza, mliu ndi khangaza pa mkawo wa mwinjiro
pozungulira, kutumikira nazo; monga Yehova anamuuza Mose.
27Ndipo anaomba maraya a bafuta, a nchito yoomba, a Aroni, ndi a ana ace
amuna, 28ndi nduwira va bafuta wa thonje losansitsa, ndi akapal okometsetsa a
bafuta wa thonje losansitsa, ndi zobvala za kumiyendo za bafuta wa thonje
losansitsa, 29ndi mpango wabafuta wa thonje losansitsa, ndi lamadzi, ndi
lofiirira, ndi lofiira, nchito ya wopikula; monga Yehova adamuuza Mose.
30Ndipo anapanga phanthiphanthi wa korona wopatulika wa golidi woona,
nalembapo lemba, ngati malocedwe a cosindikizira, KUPATULIKIRA
YEHOVA. 31Namangako mkuzi wamadzi, kuumanga nao pamwamba pa
nduwira; monga Yehova adamuuza Mose. 32Potero anatsiriza nchito yonseya
kacisi wa cihema cokomanako; ndipo ana a Israyeli adacita monga mwa zonse
Yehova adamuuza Mose, anacita momwemo.

Zopangidwa zonae zionetsedwa kwa Mose

33Ndipo anabwera naye kacisi kwa Mose, cihemaco, ndi zipangizo zace zonse,
zokowera zace, matabwa ace, mitanda yace, ndi mizati yace, nsanamira zace
ndi nsici zace, ndi makamwa ace; 34ndi cophimba ca zikopa za nkhosa
zamphongo zonika zofiirira, ndi cophimba ca zikopa za akatumbu, ndi nsaru
yocinga yotsekera; 35likasa la mboni, ndi mphiko zace, ndi
cotetezerapo; 36gomelo, zipangizo zace zonse, ndi mkate
woonekera; 37coikapo nyali coona, nyali zace, ndizo nyali zimakonzekazi, ndi
zipangizo zace zonse, ndi mafuta a kuunikira; 38ndi guwa la nsembe lagolidi,
ndi mafuta odzoza, ndi cofukiza ca pfungo lokoma, ndi nsaru yotsekera pa
khomo la cihemaco; 39guwa la nsembe lamkuwa, ndi made ace amkuwa,
mphiko zace, ndi zipangizo zace zonse, mkhate ndi tsinde lace; 40nsaru
zocingira za pabwalo, osici zace, ndi makamwa ace, ndi nsaru yotsekera pa
cipata ca pabwalo, zingwe zace, ndi ziciri zace, ndi zipangizo zonse za nchito
ya kacisi, za ku cihema cokomanako; 41zobvala zokoma za kutumikira nazo
m'malo opatulika, ndi zobvala zopatulika za Aroni wansembe, ndi zobvala za
ana ace, kucita nazo nchito ya usembe. 42Monga mwa zonse Yehova
adamuuza Mose, momwemo ana a Israyeli anacita nchito zonse. 43Ndipo
Mose anaona nchito zonse, ndipo, taonani, adaicita monga Yehova adamuuza,
momwemo adacita. Ndipo Mose anawadalitsa.

Eksodo 40
Mose autsa cihemaco
1Ndipo Yehova ananena ndi Mose, ndi kuti, 2Tsiku loyamba la mwezi woyamba
ukautse kacisi wa cihema cokomanako. 3Ndipo ukaikemo likasa la mboni,
nucinge likasalo ndi nsaru yocingayo. 4Ulongenso gomelo, nukonzerepo
zokonzera zace; ulongenso coikapo nyalico, ndi kuyatsa nyali zace. 5Ndipo
ukaike guwa la nsembe lofukizapo lazolidi cakuno ca likasa la mboni, numange
pakacisi nsaru yotsekera pakhomo. 6Ndipo ukaike guwa la nsembe yopsereza
kunja kwa khomo la kacisi wa cihema cokomanako. 7Ukaikenso mkhate pakati
pa cihema cokomanako, ndi guwa la nsembe, ndi kuthiramo madzi. 8Ndipo
ukamange mpandawo pozungulira, ndi kupacika nsaru yotsekera pa cipata ca
pabwalo. 9Pamenepo ukatenge mafuta odzoza, ndi kudzoza nao kacisi, ndi
zonse ziri m'mwemo, ndi kumpatula, ndi zipangizo zace zonse; ndipo adzakhala
wopatulika. 10Ndipo udzoze guwa la nsembe yopsereza, ndi zipangizo zace
zonse, ndi kulipatula guwalo; ndipo guwalo lidzakhala
lopatulikitsa. 11Udzozenso mkhate ndi tsinde lace, ndi kuupatula. 12Ndipo
ubwere nao Aroni ndi ana ace amuna ku khomo la cihema cokomanako, ndi
kuwasambitsa ndi madzi. 13Nubveke Aroni cobvala zopatulikazo; ndi
kumdzoza, ndi kumpatwa andicitire Ine nchito ya nsembe. 14Ndipo ubwere nao
ana ace amuna ndi kuwabveka maraya am'kati; 15nuwadzoze, monga
unadzoza atate wao, kuti andicitire nchito ya nsembe; ndi kudzozedwa kwao
kuwakhalire unsembe wosatha mwa mibadwo yao. 16Anatero Mose; monga
mwa zonse Yehova adamuuza, momwemo anacita.
17Ndipo kunali, mwezi woyamba wa caka caciwiri, tsiku loyamba la mwezi,
anautsa kacisi. 18Ndipo Mose anautsa kacisi, nakhazika makamwa ace,
naimika matabwa ace, namangapo mitanda yace, nautsa mizati ndi nsanamira
zace. 19Ndipo anayalika hema pamwamba pa kacisi, naika cophimba ca
cihema pamwamba pace; monga Yehova adamuuza Mose. 20Ndipo anatenga
mboniyo, naiika mlikasa, napisa mphiko palikasa, naika cotetezerapo
pamwamba pa likasa; 21nalowa nalo likasa m'kacisi, napacika nsaru yocinga,
nacinga likasa la mboni; monga Yehova adamuuza Mose. 22Ndipo anaika
gomelo m'cihema cokomanako, pa mbali ya kumpoto ya kacisi, kunja kwa
nsaru yocinga. 23Nakonzerapo mkate pamaso pa Yehova; monga Yehova
adamuuza Mose. 24Ndipo anaika coikapo nyali m'cihema cokomanako,
popenyana ndi gome, pa mbali ya kumwela ya kacisi. 25Nayatsa nyalizo
pamaso pa Yehova; monga Yehova adamuuza Mose. 26Ndipo anaika guwa la
nsembe lagolidi m'cihema cokomanako cakuno ca nsaru yocinga; 27nafukizapo
cofukiza ca pfungo lokoma; monga Yehova adamuuza Mose. 28Ndipo
anapacika kukacisi nsaru yotsekera pakhomo. 29Ndipo anaika guwa la nsembe
yopsereza pa khomo la kacisi wa cihema cokomanako, natenthapo nsembe
yopsereza, ndi nsembe yaufa; monga Yehova adamuuza Mose. 30Ndipo anaika
mkhate pakati pa cihema cokomanako, ndi guwa la nsembe; nathiramo madzi
osamba. 31Ndipo Mose ndi Aroni ndi ana ace amuna anasamba manja ao ndi
mapazi ao m'menemo; 32pakulowa iwo m'cihema cokomanako, ndi
pakuyandikiza guwa la nsembe anasamba; monga Yehova adamuuza
Mose. 33Ndipo anautsa mpanda pozungulira pa cihema ndi guwa la nsembe,

napacika nsaru yotsekera pa cipata ca pabwalo. Momwemo Mose anatsiriza nchitoyi.
34Pamenepo mtambo unaphimba cihema cokomanako, ndi ulemerero wa Yehova unadzaza kacisiyo. 35Ndipo Mose sanathe kulowa m'cihema cokomanako, popeza mtambo unakhalabe pamenepo; ndi ulemerero wa Yehova unadzaza kacisi. 36Ndipo pakukwera mtambo kucokera kukacisi, ana a Israyeli amayenda maulendo ao onse; 37koma ukapanda kukwera mtambo, samayenda ulendo wao kufikira tsiku loti wakwera. 38Pakuti mtambo wa Yehova unakhala pakacisi msana, ndi usiku munali moto m'menemo, pamaso pa mbumba yonse ya Israyeli, m'maulendo ao onse.

Leviticus

Levitiko 1

Za nsembe yopsereza

1NDIPO Yehova anaitana Mose, nanena naye ali m'cihema cokomanako iye,
nati, 2Lankhula ndi ana a Israyeli, nunene nao, Ali yense mwa inu akabwera
naco copereka ca kwa Yehova, muzibwera naco copereka canu cikhale ca
zoweta, ca ng'ombe, kapena ca nkhosa, kapena ca mbuzi.
3Copereka cace cikakhala nsembe yopsereza ya ng'ombe, azibwera nayo
yaimuna yopanda cirema; abwere nayo ku khomo la cihema cokomanako, kuti
alandirike pamaso pa Yehova. 4Ndipo aike dzanja lace pamutu pa nsembe
yopsereza; ndipo idzalandiridwa m'malo mwace, imtetezere. 5Pamenepo
aiphe ng'ombeyo pamaso pa Yehova; ndipo ana a Aroni, ansembewo, abwere
nao mwazi, nawaze mwaziwo pozungulira pa guwa la nsembe, lokhala pa
khoma la cihema cokomanako. 6Ndipo asende nsembe yopsereza, ndi
kuikadzula ziwalo zace. 7Ndipo ana a Aroni asonkhe mota pa guwa la nsembe,
ndi kukonza nkhuni pamotopo; 8ndi ana a Aroni, ansembewo, akonze
ziwalozo, mutu, ndi mafuta pa nkhuni ziri pa mota wa pa guwa la
nsembe; 9koma atsuke ndi madzi matumbo ace ndi miyendo yace; ndi
wansembe atenthe zonsezi pa guwa la nsembe, zikhale nsembe yopsereza,
nsembe yamoto, ya pfungo lokoma la kwa Yehova.
10Ndipo copereka cace cikakhala ca nkhosa, kapena ca mbuzi, cikhale
nsembe yopsereza; azibwera nayo yaimuna yopanda cirema. 11Ndipo aiphere
iyo pa mbali ya kumpoto ya guwa la nsembe, pamaso pa Yehova; ndipo ana a
Aroni, ansembewo, awaze mwazi wace pa guwa la nsembe
pozungulira. 12Ndipo aikadzule ziwalo zace, pamodzi ndi mutu wace ndi
mafuta ace; ndi wansembeyo akonze izi pa nkhuni ziri pa mota wa pa guwa la
nsembe. 13Koma atsuke ndi madzi matumbo ndi miyendo; ndi wansembe
abwere nazo zonse nazitenthe pa guwa la nsembe; ndiyo nsembe yopsereza,
nsembe yamoto, ya pfungo lokoma la kwa Yehova. 14Ndipo copereka cace ca
kwa Yehova cikakhala nsembe yopsereza ya mbalame, azibwera naco
copereka cace cikhale ca njiwa, kapena ca maunda. 15Ndipo wansembe
abwere naco ku guwa la nsembe, namwetule mutu wace, naitenthe pa guwa
la nsembe; ndi mwazi wace aukamulire pa mbali ya guwa la
nsembe, 16nacotse citsokomero, ndi cipwidza cace, nazitaye kufupi kwa guwa
la nsembe, kum'mawa, kudzala; 17nang'ambe mapiko ace osawacotsa konse
ai; ndipo wansembeyo aitenthe pa guwa la nsembe, pa nkhuni ziri pamoto;
ndiyo nsembe yopsereza, nsembe yamoto, ya pfungo lokoma la kwa Yehova.

Za nsembe yaufa ndi ya zipatso zoyamba

1Ndipo munthu akabwera naco copereka ndico nsembe yaufa ya kwa Yehova,
copereka cace cizikhala ca ufa wosalala; ndipo athirepo mafuta, ndi kuikapo
libano. 2Ndipo abwere nayo kwa ana a Aroni, ansembewo; natengeko ufa, ndi
mafuta odzala manja, ndi libano wace wonse; ndipo wansembeyo aitenthe
cikumbutso cace pa guwa la nsembe, ndiyo nsembe yamoto, ya pfungo
lokoma la kwa Yehova. 3Ndipo cotsalira ca nsembe yaufa cikhale ca Aroni ndi
ana ace; ndico copatulikitsa ca nsembe zamoto za Yehova.
4Ndipo ukabwera naco copereka ndico nsembe yaufa, yophika mumcembo,
cizikhala ca timitanda ta ufa wosalala topanda cotupitsa tosanganiza ndi
mafuta, kapena timitanda taphanthi topanda cotupitsa todzoza ndi
mafuta. 5Ndipo nsembe yaufa yako ikakhala yokazinga m'ciwaya, ikhale ya
ufa wosalala wopanda cotupitsa, wosanganiza ndi mafuta. 6Uphwanye,
nuthirepo mafuta; ndiyo nsembe yaufa. 7Ndipo copereka cako cikakhala
nsembe yaufa ya mumphika, cikhale ca ufa wosalala ndi mafuta. 8Ndipo
ubwere nayo nsembe yaufa yopangika ndi izi kwa Yehova; ndipo atabwera
naco kwa wansembe, iyeyo apite naco ku guwa la nsembe. 9Ndipo
wansembeyo atengeko cikumbutso pa nsembe yaufa, nacitenthe pa guwa la
nsembe; ndico nsembe yamoto ya pfungo lokoma la kwa Yehova. 10Ndipo
cotsalira ca nsembe yaufa cikhale ca Aroni ndi ana ace; ndico copatulikitsa ca
nsembe zamoto za Yehova. 11Nsembe iri yonse yaufa, imene mubwera nayo
kwa Yehova, isapangike ndi cotupitsa, pakuti musamatenthera Yehova
nsembe yamoto yacotupitsa, kapena yauci. 12Monga copereka ca zipatso
zoyamba muzipereka izi: koma asazifukize pa guwa la nsembe zicite pfungo
lokoma. 13Ndipo copereka cako ciri conse ca nsembe yaufa uzicikoleretsa ndi
mcere; usasowe mcere wa cipangano ca Mulungu wako pa nsembe yako
yaufa; pa zopereka zako zonse uzipereka mcere.
14Ndipo ukabwera nayo nsembe yaufa ya zipatso zoyamba kwa Yehova,
uzibwera nayo nsembe yako ya zipatso zoyamba ikhale ya ngala zoyamba
kuca, zoumika pamoto, zokonola. 15Ndipo uthirepo mafuta, ndi kuikapo
libona; ndiyo nsembe yaufa. 16Ndipo wansembe atenthe cikumbutso cace,
atatapa pa tirigu wace wokonola, ndi pa mafuta ace, ndi kutenga libano lace
lonse; ndiyo nsembe yamoto ya kwa Yehova.

Za nsembe yoyamika

1Ndipo copereka cace cikakhala nsembe yoyamika; akabwera nayo ng'ombe,
kapena yaimuna kapena yaikazi, azibwera nayo yopanda cirema pamaso pa
Yehova. 2Ndipo aike dzanja lace pa mutu wa copereka cace, ndi kuipha pa
cipata ca cihema cokomanako; ndipo ana a Aroni, ansembewo, awaze mwazi
wace pa guwa la nsembe pozungulira. 3Pamenepo abwere nayo nsembe
yamoto ya kwa Yehova, yotengako ku nsembe yoyamika; acotse mafuta
akukuta matumbo, ndi mafuta onse akukhala pamatumbo, 4ndi imso ziwiri,
ndi mafuta ali pomwepo okhala m'cuuno, ndi cokuta ca mphafa cofikira
kuimso. 5Ndipo ana a Aroni azitenthe pa guwa la nsembe, pa nsembe
yopsereza, iri pa nkhuni zimene ziri pamoto; ndiyo nsembe yamoto, ya pfungo
lokoma la kwa Yehova.
6Ndipo copereka cace cikakhala nkhosa kapena mbuzi, kuti ikhale nsembe
yoyamika ya kwa Yehova; ingakhale yaimuna kapena yaikazi, azibwera nayo
yopanda cirema; 7akabwera nayo nkhosa kuti ikhale copereka cace, abwere
nayo pamaso pa Yehova; 8naike dzanja lace pamutu pa copereka cace, naiphe
patsogolo pa cihema cokomanako; ndipo ana a Aroni awaze mwazi wace pa
guwa la nsembe pozungulira. 9Pamenepo abwere nayo nsembe yamoto ya
kwa Yehova; yotengako ku nsembe yoyamika; mafuta ace, mcira wamafuta
wonse, ataucotsa kufupi ku pfupa lao msana; naicotse mafuta akukuta
matumbo, ndi mafuta onse akukhala pamatumbo, 10ndi imso ziwiri, ndi
mafuta ali pomwepo, okhala m'cuuno, ndi cokuta ca mphafa cofikira
kuimso. 11Ndipo wansembe azitenthe pa guwa la nsembe; ndico cakudya ca
nsembe yamoto ya kwa Mulungu.
12Ndipo copereka cace cikakhala mbuzi, azibwera nayo pamaso pa
Yehova; 13naike dzanja lace pamutu pace, naiphe pa khomo la cihema
cokomanako; ndipo ana a Aroni awaze mwazi wace pa guwa la nsembe
pozungulira. 14Ndipo abwere naco copereka cace cotengako, ndico nsembe
yamoto ya kwa Yehova; acotse mafuta akukuta matumbo, ndi mafuta onse
akukhala pamatumbo, 15ndi imso ziwiri, ndi mafuta ali pomwepo, okhala
m'cuuno, ndi cokuta ca mphafa cofikira kuimso. 16Ndipo wansembe atenthe
izi pa guwa la nsembe; ndizo cakudya ca nsembe yamoto icite pfungo lokoma;
mafuta onse nga Yehova. 17Likhale lemba losatha m'mibadwo yanu
m'nyumba zanu zonse, musamadya kapena mafuta kapena mwazi.

Za nsembe yaucimo pocimwa wansembe

1Ndipo Yehova ananena ndi Mose, nati, 2Lankhula ndi ana a Israyeli, ndi kuti, Munthu akacimwa, osati dala, pa cina ca zinthu ziri zonse aziletsa Mulungu, nakacitapo kanthu; 3akalakwa wansembe wodzozedwa ndi kuparamulira anthu; pamenepo azibwera nayo kwa Yehova ng'ombe yamphongo, yopanda cirema, cifukwa ca kucimwa kwace adakucita, ikhale nsembe yaucimo. 4Ndipo adze nayo ng'ombeyo ku khomo la cihema cokomanako pamaso pa Yehova; naike dzanja lace pamutu pa ng'ombeyo, naiphe ng'ombeyo pamaso pa Yehova. 5Ndipo wansembe wodzozedwayo atengeko mwazi wa ng'ombeyo, nabwerenao ku cihema cokomanako; 6ndipo wansembeyo abviike cala cace m'mwazimo, nawaze mwaziwo kasanu ndi kawiri pamaso pa Yehova cakuno ca nsaru yocinga, ya malo opatulika. 7Ndipo wansembeyo atengeko mwazi, nauike pa nyanga za guwa la nsembe la cofukiza ca pfungo lokoma, lokhala m'cihema cokomanako pamaso pa Yehova; nathire mwazi wonse wa ng'ombeyo patsinde pa guwa la nsembe yopsereza, lokhala pa khomo la cihema cokomanako. 8Ndipo acotse mafuta onse a ng'ombe ya nsembe yaucimo, acotse mafuta akukuta matumbo, ndi mafuta onse akukhala pamatumbo, 9ndi imso ziwiri ndi mafuta ali pomwepo, okhala m'cuuno, ndi cokuta ca mphafa cofikira kuimso, 10umo azikacotsera pa ng'ombe ya nsembe yoyamika; ndipo wansembe azitenthe pa guwa la nsembe yopsereza. 11Naturutse cikopa ca ng'ombeyo, ndi nyama yace yonse, pamodzi ndi mutu wace, ndi miyendo yace, ndi matumbo ace, ndi cipwidza cace, 12inde ng'ombe yonse, kunja kwa cigono, kumka nayo kumalo koyera, kumene atayako mapulusa, naitenthe pankhuni ndi moto; aitenthe potayira mapulusa.

Za nsembe yaucimo pocimwa mtundu wonse wa Israyeli

13Ndipo khamu lonse la Israyeli likalakwa osati dala, ndipo cikabisika cinthuci pamaso pa msonkhano, litacita cina ca zinthu ziri zonse aziletsa Yehova, ndi kuparamula; 14kukadziwika kucimwa adacimwako, pamenepo msonkhano uzibwera nayo ng'ombe yamphongo, ikhale nsembe yaucimo, ndipo udze nayo ku khomo la cihema cokomanako. 15Ndipo akuru a khamulo aike manja ao pamutu pa ng'ombeyo, pamaso pa Yehova; naiphe ng'ombeyo pamaso pa Yehova. 16Ndipo wansembe wodzozedwayo adze nao mwazi wina wa ng'ombeyo ku cihema cokomanako; 17nabviike cala cace m'mwazi wa nsembewo, nauwaze kasanu ndi kawiri pamaso pa Yehova, cakuno ca nsaru yocinga. 18Naike mwazi wina pa nyanga za guwa la nsembe, lokhala pamaso pa Yehova, lokhala m'cihema cokomanako; nathire mwazi wonse patsinde pa guwa la nsembe yopsereza, lokhala pa khomo la cihema cokomanako. 19Ndipo acotse mafuta ace onse, nawatenthe pa guwa la nsembe. 20Atero nayo ng'ombeyo; monga umo anacitira ng'ombe ya nsembe yaucimo; ndipo wansembe awacitire cowatetezera, ndipo adzakhululukidwa. 21Ndipo aturutse ng'ombeyo kunja kwa cigono, ndi kuitentha monga anatenthera ng'ombe yoyamba ija; ndiyo nsembe yaucimo ya kwa msonkhano.

Za nsembe yaucimo pocimwa mkuru

22Akacimwa mkuru, osati dala, pa cina ca zinthu ziti zonse aziletsa Yehova Mulungu wace, naparamula; 23akamdziwitsa kucimwa kwace adacimwako, azidza naco copereka cace, ndico tonde wopanda cirema; 24naike dzanja lace pamutu pa mbuziyo, naiphe pamalo pophera nsembe yopsereza pamaso pa Yehova; ndiyo nsembe yaucimo. 25Ndipo wansembe atengeko mwazi wa nsembe yaucimo ndi cala cace, nauike pa nyanga za guwa la nsembe

yopsereza, ndi kuthira mwazi wace patsinde pa guwa la nsembe yopsereza. 26Ndipo atenthe mafuta ace onse pa guwa la nsembe, monga mafuta a nsembe yoyamika; ndipo wansembe amcitire comtetezera, ndipo adzakhululukidwa.

Za nsembe yaucimo pocimwa munthu yekha

27Ndipo akacimwa wina wa anthu a m'dziko, osati dala, pa cina ca zinthu ziri zonse aziletsa Yehova, naparamula; 28akamdziwitsa kucimwa kwace adacimwako, azidza naco copereka cace mbuzi yaikazi, yopanda cirema, cifukwa ca kucimwa kwace adakucita. 29Aike dzanja lace pamutu pa nsembe yaucimo, naiphe nsembe yaucimo pamalo pa nsembe yopsereza. 30Ndipo wansembe atengeko mwazi ndi cala cace, nauike pa nyanga za guwa la nsembe yopsereza, ndi kuthira mwazi wace wonse patsinde pa guwa la nsembe. 31Nacotse mafuta ace onse, monga umo amacotsera mafuta pa nsembe yoyamika; ndipo wansembeyo awatenthe pa guwa la nsembe akhale pfungo lokoma la kwa Yehova; ndi wansembe amcitire comtetezera, ndipo adzakhululukidwa.

32Ndipo akadza nayo nkhosa, ndiyo copereka cace, ikhale nsembe yaucimo, azidza nayo yaikazi, yopanda cirema. 33Naike dzanja lace pa mutu wa nsembe yaucimo, ndi kuipha ikhale nsembe yaucimo pamalo pophera nsembe yopsereza. 34Ndipo wansembe atengeko mwazi wa nsembe yaucimo ndi cala cace, nauike pa nyanga za guwa la nsembe yopsereza, ndi kuthira mwazi wace wonse patsinde pa guwa la nsembe; 35nawacotse mafuta ace onse, monga umo amacotsera mafuta a nkhosa pa nsembe yoyamika; ndipo wansembeyo atenthe, awa pa guwa la nsembe, monga umo amacitira nsembe zamoto za Yehova; ndipo wansembeyo amcitire comtetezera pa kucimwa kwace adakucimwira, ndipo adzakhululukidwa.

Za nsembe yoparamula

1Ndipo akacimwa munthu, wakuti adamva mau akuwalumbiritsa, ndiye
mboni, kapena wakuona, kapena wakudziwa, koma osaulula, azisenza
mphulupulu yace; 2kapena munthu akakhudza ciri conse codetsa kapena
mtembo wa nyama yodetsa, kapena mtembo wa coweta codetsa, kapena
mtembo wa cokwawa codetsa, kungakhale kudambisikira, ali wodetsedwa, ndi
woparamula. 3Kapena akakhudza codetsa ca munthu, ndico codetsa ciri conse
akakhala codetsedwa naco, ndipo cidambisikira; koma pocizindikira akhala
woparamula: 4kapena munthu akalumbira ndi milomo yace osalingirira kucita
coipa, kapena kucita cabwino, ciri conse munthu akalumbira osalingirira,
ndipo cidambisikira; koma pocizindikira akhala woparamula cimodzi ca
izi: 5ndipo kudzali, ataparamula cimodzi ca izi, aziulula cimene adacimwa
naco; 6nadze nayo nsembe yoparamula kwa Yehova cifukwa ca kulakwa
kwace adacimwira, ndiyo msoti wa nkhosa, kapena msoti wa mbuzi, ukhale
nsembe yaucimo; ndipo wansembe amcitire comtetezera cifukwa ca kucimwa
kwace. 7Ndipo cuma cace cikapanda kufikira nkhosa, wocimwayo adze nayo
kwa Yehova nsembe yace yoparamula, njiwa ziwiri, kapena maunda awiri;
imodzi ikhale ya nsembe yaucimo, ndi yina ya nsembe yopsereza. 8Ndipo
adze nazo kwa wansembe, ndiye ayambe kubwera nayo ija ya kwa nsembe
yaucimo, napotole mutu wace pakhosi pace, osaucotsa; 9nawazeko mwazi wa
nsembe yaucimo pa mbali ya guwa la nsembe; ndi mwazi wotsalira
aukamulire patsinde pa guwa la nsembe; ndiyo nsembe yaucimo. 10Ndipo
aikonze inzace ikhale nsembe yopsereza, manga mwa lemba lace; ndipo
wansembe amcitire comtetezera cifukwa ca kucimwa adacimwira, ndipo
adzakhululukidwa.
11Koma cuma cace cikapanda kufikira njiwa ziwiri kapena maunda awiri,
wocimwayo azidza naco copereka cace limodzi la magawo khumi la efa la ufa
wosalala, likhale la nsembe yaucima; asamaikapo mafuta, kapena kuikapo
libona ai; pakuti ndico nsembe yaucimo. 12Ndipo adze naco kwa wansembe,
ndi wansembeyo atengeko wodzala manja ukhale cikumbutso cace,
nacitenthe pa guwa la nsembe monga umo amacitira nsembe zamoto za
Yehova; ndiyo nsembe yaucimo. 13Ndipo wansembe amcitire comtetezera
cifukwa ca kucimwa kwace adacimwira cimodzi ca izi, ndipo
adzakhululukidwa; ndipo cotsalira cikhale ca wansembe, monga umo
amacitira copereka caufaco.
14Ndipo Yehova ananena ndi Mose, nati, 15Munthu akacita mosakhulupirika,
nakacimwa osati dala, pa zopatulika za Yehova, azidza nayo nsembe yace
yoparamula kwa Yehova, ndiyo nkhosa yamphongo yopanda cirema, ya
m'gulu lace, monga umayesa mtengo wace pochula masekeli a siliva, kunena
sekeli wa malo opatulika, ikhale nsembe yoparamula; 16ndipo abwezere
colakwira copatulikaco, naonjezepo limodzi la magawo asanu, napereke kwa
wansembe; ndi wansembeyo amcitire comtetezera ndi nkhosa yamphongo ya
nsembe yoparamula; ndipo adzakhululukidwa.
17Ndipo munthu akacimwa, nakacita dna ca zinthu ziti zonse aziletsa Yehova;
angakhale analibe kudziwa, koma waparamula, azisenza mphulupulu
yace. 18Nadze nayo kwa wansembe nkhosa yamphongo yopanda cirema ya
m'khola lace, monga umayesa mtengo wace, ikhale nsembe yoparamula;
ndipo wansembeyo amcitire comtetezera cifukwa ca kusacimwa dala kwace,
osakudziwa; ndipo adzakhululukidwa. 19Iyo ndiyo nsembe yoparamula;
munthuyu anaparamula ndithu pamaso pa Yehova.

Cilamulo ca nsembe yo paramula

1Ndipo cilamulo ca nsembe yoparamula ndi ici: ndiyo yopatulikitsa. 2Pamalo
pophera nsembe yopsereza ndipo aziphera nsembe yoparamula; nawaze
mwazi wace pa guwa la nsembe pozungulira. 3Ndipo acotseko, nabwere nao
mafuta ace onse; mcira wamafuta, ndi mafuta akukuta matumbo, 4ndi imso
ziwiri, ndi mafuta a pamenepo, okhala m'cuuno, ndi cokuta ca mphafa cofikira
kuimso; 5ndipo wansembe atenthe izi pa guwa la nsembe, nsembe yamoto ya
kwa Yehova; ndiyo nsembe yoparamula. 6Amuna onse a mwa ansembe
adyeko; adyere m'malo opatulika; ndiyo yopatulikitsa. 7Monga nsembe
yaucimo, momwemo nsembe yoparamula; pa zonse ziwirizi pali cilamulo
cimodzi; ikhale yace ya wansembeyo, amene acita nayo cotetezera. 8Ndipo
cikopa ca nsembe yopsereza cikhale cace cace ca wansembe, amene
anabwera nayo nsembe yopsereza ya munthu ali yense. 9Ndipo nsembe zaufa
zonse zophika mumcembo, ndi zonse zokonzeka mumphika, ndi paciwaya,
zikhale za wansembe amene wabwera nazo, 10Ndipo nsembe zonse zaufa
zosanganiza ndi mafuta, kapena zouma zikhale za ana onse a Aroni,
alandireko onse.

Cilamulo ca nsembe yoyamika

11Ndipo cilamulo ca nsembe zoyamika, zimene azibwera Daze kwa Yehova ndi
ici: 12akabwera nayo kuti ikhale nsembe yolemekeza, azibwera nato, pamodzi
ndinsembe yolemekeza, timitanda topanda cotupitsa tosanganiza ndi mafuta,
ndi timitanda taphanthi topanda cotupitsa todzoza ndi mafuta, ndi timitanda
tooca, ta ufa wosalala tosanganiza ndi mafuta. 13Abwere naco copereka cace
pamodzi ndi timitanda ta mkate wacotupitsa, pamodzi ndi nsembe
yolemekeza, ya nsembe zoyamika zace. 14Ndipo pa zopereka zonsezi
atengepo ndi kubwera nako kamtanda kamodzi, kuti kakhale ka nsembe
yokweza ya kwa Yehova; kakhale ka wansembe wakuwaza mwazi wa nsembe
zoyamika. 15Kunena za nyama ya nsembe volemekeza ya nsembe zoyamika
zace, aziidya tsiku lomwelo lakuipereka; asasiyeko kufikira m'mawa. 16Koma
nsembe ya copereka cace ikakhala ya cowinda, kapena copereka caufuhi,
aidye tsiku lomwelo anabwera nayo nsembe yace; ndipo m'mawa adye
cotsalirapo; 17koma cotsalira pa nyama ya nsembeyo tsiku lacitatu,
acitenthe. 18Ndipo akadyako nyama ya nsembe zoyamika zace tsiku lacitatu,
sikubvomerezeka kumene; sadzamwerengera wobwera nayo; ndiyo cinthu
conyansa, ndipo munthu wakudyako adzasenza mphulupulu zace. 19Ndipo
nyama yokhudza kanthu kali konse kodetsa isadyeke; aitenthe ndi moto.
Koma za nyama yina, ali yense ayera aidyeko. 20Koma munthu akadya nyama
ya nsembe zoyamika za Yehova, pokhala naco comdetsa, munthuyo
asadzidwe kwa anthu a mtundu wace. 21Ndipo munthu akakhudza cinthu
codetsa, codetsa ca munthu, kapena codetsa ca zoweta, kapena ciri conse
conyansa codetsa, nakadyako nyama ya nsembe zoyamika za Yehova,
munthuyo asadzidwe kwa anthu a mtundu wace.

Aletsedwa asadye mafuta ndi mwazi

22Ndipo Yehova ananena ndi Mose, nati, 23Lankhula ndi ana a Israyeli ndi kuti,
Musamadya mafuta ali onse, a ng'ombe, kapena a nkhosa, kapena a
mbuzi. 24Ndipo mafuta a iyo idafa yokha, ndi mafuta a iyo idajiwa ndi cirombo
ayenera nchito iri yonse, koma musamadya awa konse konse. 25Pakuti ali
yense akadya mafuta a nyama imene amabwera nayo ikhale nsembe yamoto
ya kwa Yehova, munthu amene akadya awa asadzidwe kwa anthu a mtundu
wace. 26Ndipo musamadya mwazi uti wonse, kapena wa mbalame, kapena wa

nyama, m'nyumba zanu zonse, 27Ali yense akadya mwazi uti wonse,
munthuyo asadzidwe kwa anthu a mtundu wace.

Za gawo la ansembe

28Ndipo Yehova ananena ndi Mose, nati, 29Lankhula ndi ana a Israyeli, ndi
kuti, Wakubwera nayo nsembe yoyamika yace kwa Yehova, azidza naco
copereka cace kwa Yehova cocokera ku nsembe yoyamika yace; 30adze nazo
m'manja mwace nsembe zamoto za Yehova; adze nao mafuta pamodzi ndi
nganga, kuti aweyule ngangayo ikhale nsembe yoweyula pamaso pa
Yehova. 31Ndipo wansembeyo atenthe mafutawo pa guwa la nsembe; koma
ngangayo ikhale ya Arent ndi ana ace. 32Ndipo mwendo wathako wa ku
dzanja lamanja muupereke kwa wansembe, ukhale nsembe yokweza yocokera
ku nsembe zoyamika zanu. 33Mwendo wathako wa ku dzanja lamanja ukhale
gawo lace la iyeyu mwa ana a Aroni wakubwera Ilao mwazi wa zopereka
zoyamika, ndi mafuta. 34Pakuti ndatengako kwa ana a Israyeli, ku nsembe
zoyamika zao, nganga ya nsembe yoweyula, ndi mwendo wathako wa ku
dzanja lamanja wa nsembe yokweza; ndipo ndazipereka kwa Aroni wansembe
ndi kwa ana ace, zikhale zoyenera iwo kosatha zocokera kwa ana a Israyeli.
35Ili ndi gawo la Aroni, ndi gawo la ana ace, locokera ku nsembe zamoto za
Yehova, analinena, tsiku limene iye anawasendeza alowe utumiki wa ansembe
a Yehova; 36limene Yehova anauza ana a Israyeli aziwapatsa, tsiku limene iye
anawadzoza. Likhale lemba losatha mwa mibadwo yao. 37Ico ndi cilamulo ca
nsembe yopsereza, ca nsembe yaufa, ca nsembe yaucimo, ndi ca nsembe
yoparamula, ndi ca kudzaza dzanja, ndi ca nsembe zoyamika; 38cimene
Yehova analamulira Mose m'phiri la Sinai, tsikuli anauza ana a Israyeli abwere
nazo zopereka zao kwa Yehova, m'cipululu ca Sinai.

Cilamulo ca nsembe yo paramula

1Ndipo cilamulo ca nsembe yoparamula ndi ici: ndiyo yopatulikitsa. 2Pamalo pophera nsembe yopsereza ndipo aziphera nsembe yoparamula; nawaze mwazi wace pa guwa la nsembe pozungulira. 3Ndipo acotseko, nabwere nao mafuta ace onse; mcira wamafuta, ndi mafuta akukuta matumbo, 4ndi imso ziwiri, ndi mafuta a pamenepo, okhala m'cuuno, ndi cokuta ca mphafa cofikira kuimso; 5ndipo wansembe atenthe izi pa guwa la nsembe, nsembe yamoto ya kwa Yehova; ndiyo nsembe yoparamula. 6Amuna onse a mwa ansembe adyeko; adyere m'malo opatulika; ndiyo yopatulikitsa. 7Monga nsembe yaucimo, momwemo nsembe yoparamula; pa zonse ziwirizi pali cilamulo cimodzi; ikhale yace ya wansembeyo, amene acita nayo cotetezera. 8Ndipo cikopa ca nsembe yopsereza cikhale cace cace ca wansembe, amene anabwera nayo nsembe yopsereza ya munthu ali yense. 9Ndipo nsembe zaufa zonse zophika mumcembo, ndi zonse zokonzeka mumphika, ndi paciwaya, zikhale za wansembe amene wabwera nazo, 10Ndipo nsembe zonse zaufa zosanganiza ndi mafuta, kapena zouma zikhale za ana onse a Aroni, alandireko onse.

Cilamulo ca nsembe yoyamika

11Ndipo cilamulo ca nsembe zoyamika, zimene azibwera Daze kwa Yehova ndi ici: 12akabwera nayo kuti ikhale nsembe yolemekeza, azibwera nato, pamodzi ndinsembe yolemekeza, timitanda topanda cotupitsa tosanganiza ndi mafuta, ndi timitanda taphanthi topanda cotupitsa todzoza ndi mafuta, ndi timitanda tooca, ta ufa wosalala tosanganiza ndi mafuta. 13Abwere naco copereka cace pamodzi ndi timitanda ta mkate wacotupitsa, pamodzi ndi nsembe yolemekeza, ya nsembe zoyamika zace. 14Ndipo pa zopereka zonsezi atengepo ndi kubwera nako kamtanda kamodzi, kuti kakhale ka nsembe yokweza ya kwa Yehova; kakhale ka wansembe wakuwaza mwazi wa nsembe zoyamika. 15Kunena za nyama ya nsembe volemekeza ya nsembe zoyamika zace, aziidya tsiku lomwelo lakuipereka; asasiyeko kufikira m'mawa. 16Koma nsembe ya copereka cace ikakhala ya cowinda, kapena copereka caufuhi, aidye tsiku lomwelo anabwera nayo nsembe yace; ndipo m'mawa adye cotsalirapo; 17koma cotsalira pa nyama ya nsembeyo tsiku lacitatu, acitenthe. 18Ndipo akadyako nyama ya nsembe zoyamika zace tsiku lacitatu, sikubvomerezeka kumene; sadzamwerengera wobwera nayo; ndiyo cinthu conyansa, ndipo munthu wakudyako adzasenza mphulupulu zace. 19Ndipo nyama yokhudza kanthu kali konse kodetsa isadyeke; aitenthe ndi moto. Koma za nyama yina, ali yense ayera aidyeko. 20Koma munthu akadya nyama ya nsembe zoyamika za Yehova, pokhala naco comdetsa, munthuyo asadzidwe kwa anthu a mtundu wace. 21Ndipo munthu akakhudza cinthu codetsa, codetsa ca munthu, kapena codetsa ca zoweta, kapena ciri conse conyansa codetsa, nakadyako nyama ya nsembe zoyamika za Yehova, munthuyo asadzidwe kwa anthu a mtundu wace.

Aletsedwa asadye mafuta ndi mwazi

22Ndipo Yehova ananena ndi Mose, nati, 23Lankhula ndi ana a Israyeli ndi kuti, Musamadya mafuta ali onse, a ng'ombe, kapena a nkhosa, kapena a mbuzi. 24Ndipo mafuta a iyo idafa yokha, ndi mafuta a iyo idajiwa ndi cirombo ayenera nchito iri yonse, koma musamadya awa konse konse. 25Pakuti ali yense akadya mafuta a nyama imene amabwera nayo ikhale nsembe yamoto ya kwa Yehova, munthu amene akadya awa asadzidwe kwa anthu a mtundu wace. 26Ndipo musamadya mwazi uti wonse, kapena wa mbalame, kapena wa

nyama, m'nyumba zanu zonse, 27Ali yense akadya mwazi uti wonse,
munthuyo asadzidwe kwa anthu a mtundu wace.

Za gawo la ansembe

28Ndipo Yehova ananena ndi Mose, nati, 29Lankhula ndi ana a Israyeli, ndi
kuti, Wakubwera nayo nsembe yoyamika yace kwa Yehova, azidza naco
copereka cace kwa Yehova cocokera ku nsembe yoyamika yace; 30adze nazo
m'manja mwace nsembe zamoto za Yehova; adze nao mafuta pamodzi ndi
nganga, kuti aweyule ngangayo ikhale nsembe yoweyula pamaso pa
Yehova. 31Ndipo wansembeyo atenthe mafutawo pa guwa la nsembe; koma
ngangayo ikhale ya Arent ndi ana ace. 32Ndipo mwendo wathako wa ku
dzanja lamanja muupereke kwa wansembe, ukhale nsembe yokweza yocokera
ku nsembe zoyamika zanu. 33Mwendo wathako wa ku dzanja lamanja ukhale
gawo lace la iyeyu mwa ana a Aroni wakubwera Ilao mwazi wa zopereka
zoyamika, ndi mafuta. 34Pakuti ndatengako kwa ana a Israyeli, ku nsembe
zoyamika zao, nganga ya nsembe yoweyula, ndi mwendo wathako wa ku
dzanja lamanja wa nsembe yokweza; ndipo ndazipereka kwa Aroni wansembe
ndi kwa ana ace, zikhale zoyenera iwo kosatha zocokera kwa ana a Israyeli.
35Ili ndi gawo la Aroni, ndi gawo la ana ace, locokera ku nsembe zamoto za
Yehova, analinena, tsiku limene iye anawasendeza alowe utumiki wa ansembe
a Yehova; 36limene Yehova anauza ana a Israyeli aziwapatsa, tsiku limene iye
anawadzoza. Likhale lemba losatha mwa mibadwo yao. 37Ico ndi cilamulo ca
nsembe yopsereza, ca nsembe yaufa, ca nsembe yaucimo, ndi ca nsembe
yoparamula, ndi ca kudzaza dzanja, ndi ca nsembe zoyamika; 38cimene
Yehova analamulira Mose m'phiri la Sinai, tsikuli anauza ana a Israyeli abwere
nazo zopereka zao kwa Yehova, m'cipululu ca Sinai.

Kupatulidwa kwa ansembe

1Ndipo Yehova ananena ndi Mose, nati, 2Tenga Aroni ndi ana ace pamodzi naye ndi zobvalazo, ndi mafuta odzozawo, ndi ng'ombe ya nsembe yaucimoyo, ndi nkhosa zamphongo ziwirizo, ndi mtanga wa mkate wopanda cotupitsawo; 3nusonkhanitse khamu lonse ku khomo la cihema cokomanako. 4Ndipo Mose anacita monga Yehova anamuuza; ndi khamulo linasonkhana pa khomo la cihema cokomanako. 5Ndipo Mose anati kwa msonkhanowo, Ici ndi cimene Yehova adauza kuti cicitike. 6Ndipo Mose anabwera nao Aroni ndi ana ace, nawasambitsa ndi madzi, 7Ndipo anambveka ndi maraya a m'kati, nammanga m'cuuno ndi mpango, nambveka ndi mwinjiro, nambveka ndi efodi, nammanga m'cuuno ndi mpango wa efodi nammanga nao pathupi pace. 8Ndipo anamuika capacifuwa; naika m'capacifuwa Urimu ndi Tumimu. 9Naika nduwirayo pamutu pace; ndi panduwira, pamphumi pace anaika golidi waphanthiphanthi, ndiwo korona wopatulika; monga Yehova adauza Mose. 10Ndipo Mose anatenga mafuta odzoza, nadzoza kacisi, ndi ronse ziti m'mwemo, nazipatula. 11Ndipo anawazako pa guwa la nsembe kasanu ndi kawiri, nadzoza guwa la nsembe, ndi zipangizo zace zonse, ndi mkhate ndi tsinde lace, kuzipatula. 12Ndipo anatsanulirako mafuta odzoza pamutu pa Aroni, namdzoza kumpatula, 13Ndipo Mose anatenga ana a Aroni, nawabveka maraya a m'kati, nawamanga m'cuuno ndi mipango, nawamanga akapa; monga Yehova adauza Mose. 14Ndipo anabwera nayo ng'ombe ya nsembe yaucimo; ndipo Aroni ndi ana ace amuna anaika manja ao pa mutu wa ng'ombe ya nsembe yaucimo. 15Ndipo anaipha; ndi Mose anatenga mwaziwo, naupaka ndi cala cace pa nyanga za guwa la nsembe pozungulira; nayeretsa guwa la nsembe, nathira mwazi patsinde pa guwa la nsembe, nalipatula, kuti alicitire colitetezera. 16Ndipo anatenga mafuta onse a pamatumbo, ndi cokuta ca mphafa, ndi imso ziwiri, ndi mafuta ace, ndipo Mose anazitentha pa guwa la nsembe. 17Koma ng'ombeyo, ndi cikopa cace, ndi nyama yace, ndi cipwidza cace, anazitentha ndi mote kunja kwa cigono; monga Yehova adamuuza Mose. 18Ndipo anabwera nayo nkhosa yamphongo ya nsembe yopsereza; ndipo Aroni ndi ana ace amuna anaika manja ao pamutu pa mphongoyo. 19Ndipo anaipha; ndi Mose anawaza mwazi wace pa guwa la nsembe pozungulira. 20Ndipo anapadzula mphongoyo ziwalo zace; ndi Mose anatentha mutuwo ndi ziwalo, ndi mafuta. 21Koma anatsuka matumbo ndi miyendo ndi madzi; ndi Mose anatentha mphongo yonse pa guwa la nsembe; ndiyo nsembe yopsereza yocita pfungo lokoma; ndiyo nsembe yamoto ya kwa Yehova; monga Yehova adamuuza Mose.

Kupatulidwa kwa Aroni ndi ana ace

22Ndipo anabwera nayo nkhosa yamphongo yinayo, ndiyo mphongo ya kudzaza manja; ndipo Aroni ndi ana ace amuna anaika manja ao pa mutu wa mphongoyo. 23Ndipo anaipha; ndi Mose anatengako mwazi wace naupaka pa ndewerere ya khutu la ku dzanja lamanja la Aroni, ndi pa cala cacikuru ca ku dzanja lamanja lace, ndi pa cala cacikuru ca phazi lace la ku dzanja lamanja. 24Pamenepo anabwera nao ana amuna a Aroni, ndi Mose anatengako mwazi, naupaka pa ndewerere ya khutu lao la ku dzanja lamanja, ndi pa cala cacikuru ca ku dzanja lamanja lao, ndi pacala cacikuru ca phazi lao la ku dzanja lamanja; ndipo Mose anawaza mwaziwo pa guwa la nsembe pozungulira, 25Ndipo anatenga mafutawo ndi mcira wamafuta, ndi mafuta onse a pamatumbo, ndi cokuta ca mphafa, ndi imso ziwiri, ndi mafuta ace, ndi mwendo wathako wa ku dzanja lamanja; 26ndipo mu mtanga wa mkate

wopanda cotupitsa wokhala pamaso pa Yehova, anatengeramo kamtanda kamodzi kopanda cotupitsa, ndi kamtanda kamodzi ka mkate wamafuta, ndi kamtanda kamodzi kaphanthi, natiika pa mafutawo, ndi pa mwendo wathako wa ku dzanja lamanja; 27anaika zonsezi m'manja mwa Aroni, ndi m'manja mwa ana ace amuna, naziweyula nsembe yoweyula pamaso pa Yehova. 28Pamenepo Mose anazicotsa ku manja ao, nazitentha pa guwa la nsembe, pa nsembe yopsereza; ndizo nsembe zodzaza manja zocita pfungo lokoma; ndiyo nsembe yamoto ya kwa Yehova. 29Ndipo Mose anatenga ngangayo naiweyula, nsembe yoweyula pamaso pa Yehova; ndilo gawo la Mose la ku nkhosa yamphongo ya kudzaza manja; monga Yehova adamuuza Mose. 30Ndipo Mose anatengako mafuta odzoza, ndi mwazi unakhala pa guwa la nsembewo, naziwaza pa Aroni, pa zobvala zace, ndi pa ana ace amuna, ndi pa zobvala za ana ace amuna omwe; napatula Aroni, ndi zobvala zace, ndi ana ace amuna, ndi zobvala za ana ace amuna omwe. 31Ndipo Mose anati kwa Aroni ndi kwa ana ace amuna, Phikani nyamayi pakhomo pa cihema cokomanako; ndipo muidyere komweko ndi mkate uli mu mtanga wa nsembe zodzaza manja, monga ndinauza, ndi kuti, Aroni ndi ana ace aidye. 32Koma cotsalira ca nyama ndi mkate mucitenthe ndi moto. 33Ndipo musaturuka pa khomo la cihema cokomanako masiku asanu ndi awiri, kufikira anakwanira masiku a kudzaza manja kwanu; pakuti adzaze manja anu masiku asanu ndi awiri. 34Monga anacita lero lino, momwemo Yehova anauza kucita, kukucitirani cotetezera. 35Ndipo mukhale pakhomo pa cihema cokomanako masiku asanu ndi awiri, usana ndi usiku, ndi kusunga cilangizo ca Yehova, kuti mungafe; pakuti anandiuza kotero. 36Ndipo Aroni ndi ana ace amuna anacita zonse zimene Yehova anauza pa dzanja la Mose.

Aroni adziperekera yekha ndi anthu nsembe, ndizo nsembe zoyamba

1Ndipo kunali, tsiku lacisanu ndi citatu, kuti Mose anaitana Aroni ndi ana ace
amuna, ndi akuru a Israyeli; 2ndipo anati kwa Aroni, Dzitengere mwana wa
ng'ombe wamwamuna, akhale nsembe yaucimo, ndi nkhosa yamphongo
ikhale nsembe yopsereza, zopanda cirema, nubwere nazo pamaso pa
Yehova. 3Nunene kwa ana a Israyeli, ndi kuti, Dzitengereni tonde akhale
nsembe yaucimo; ndi mwana wa ng'ombe, ndi mwana wa nkhosa, a caka
cimodzi, opanda cirema, akhale nsembe yopsereza; 4ndi ng'ombe, ndi nkhosa
yamphongo zikhale zakuyamika, kuziphera nsembe pamaso pa Yehova; ndi
nsembe yaufa yosanganiza ndi mafuta; pakuti lero Yehova wakuonekerani
inu. 5Pamenepo anatenga zimene Mose anawauza, napita nazo pakhomo pa
cihema cokomanako; ndi msonkhano wonse unasendera kufupi nuimirira
pamaso pa Yehova, 6Ndipo Mose anati, Ici ndi cimene Yehova anakuuzani kuti
mucicite; ndipo ulemerero wa Yehova udzaonekera kwa inu. 7Ndipo Mose
anati kwa Aroni, Sendera kufupi kwa guwa la nsembe, nukonze nsembe yako
yaucimo, ndi nsembe yako yopsereza, nudzicitire wekha ndi anthuwo
cotetetezera; nupereke coperekaca anthu, ndi kuwacitira cotetezera; monga
Yehova anauza. 8Pamenepo Aroni anasendera kufupi kwa guwa la nsembe,
napha mwana wa ng'ombe wa nsembe yaucimo, ndiyo ya kwa iye
yekha. 9Ndipo ana a Aroni anasendera nao mwazi kwa iye; ndipo anabviika
cala cace m'mwazimo naupaka pa nyanga za guwa la nsembe, nathira
mwaziwo patsinde pa guwa la nsembe; 10koma mafutawo, ndi imso, ndi
cokuta ca mphafa za nsembe yaucimo, anazitentha pa guwa la nsembe;
monga Yehova anauza Mose. 11Ndipo anatentha ndi moto nyamayi ndi cikopa
kunja kwa cigono. 12Ndipo anapha nsembe yopsereza; ndi ana a Aroni
anapereka mwaziwo kwa iye, ndipo anauwaza pa guwa la nsembe pozu
ngulira. 13Ndipo anapereka nsembe yopsereza kwa iye, ciwalo ciwalo, ndi
mutu wace; ndipo anazitentha pa guwa la nsembe. 14Ndipo anatsuka
matumbo ndi miyendo, nazitentha pa nsembe yopsereza pa guwa la
nsembe. 15Ndipo anabwera naco copereka ca anthu, natenga mbuzi ya
nsembe yaucimo ndiyo ya kwa anthu, naipha, naipereka nsembe yaucimo,
monga yoyamba ija. 16Ndipo anabwera nayo nsembe yopsereza naipereka
monga mwa lemba lace. 17Ndipo anabwera nayo nsembe yaufa, natengako
wodzala dzanja, nautentha pa guwa la nsembe, angakhale adatentha nsembe
yopsereza ya m'mawa. 18Anaphanso ng'ombe, ndi nkhosa yamphongoyo,
ndizo nsembe zoyamika za anthu; ndi ana a Aroni anapereka kwa iye
mwaziwo, ndipo anauwaza pa guwa la nsembe pozungulira, ndi mafuta a
ng'ombe; 19ndi a nkhosa, ndi mcira wamafuta, ndi cophimba matumbo, ndi
imso, ndi cokuta ca mphafa; 20ndipo anaika mafuta pa ngangazo, natentha
mafutawo pa guwa la nsembe. 21Ndipo Aroni anaweyula ngangazo ndi
mwendo wathako wa ku dzanja lamanja zikhale nsembe yoweyula pamaso pa
Yehova; monga iye anauza Mose. 22Ndipo Aroni anakweza dzanja lace
kulozera anthu, nawadalitsa; natsika kuja anapereka nsembe yaucimo, ndi
nsembe yopsereza, ndi nsembe zoyamika. 23Ndipo Mose ndi Aroni analowa ku
cihema cokomanako, naturuka, nadalitsa anthu; ndipo ulemero wa Yehova
unaonekera kwa anthu onse. 24Ndipo unaturuka mota pamaso ya Yehova,
nunyeketsa nsembe yopsereza ndi mafuta pa guwa la nsembe; ndipo
pakuciona anthu onse anapfuula, nagwa nkhope zao pansi.

Kucimwa ndi kuphedwa kwa Nadabu ndi Abihu

1Ndipo ana a Aroni, Nadabu ndi Abihu anatenga yense mbale yace ya
zofukiza, naikamo moto, naikapo cofukiza, nabwera nao pamaso pa Yehova
moto wacilendo, umene sanawauza. 2Ndipo panaturuka moto pamaso pa
Yehova, nuwatha, nafa iwo pamaso pa Yehova. 3Ndipo Mose anati kwa Aroni,
Ici ndi cimene Yehova ananena, ndi kuti, Mwa iwo akundiyandikiza
ndipatulidwa Ine, ndi pamaso pa anthu onse ndilemekezedwa. Ndipo Aroni
anakhala cete. 4Ndipo Mose anaitana Misayeli ndi Elizafana, ana a Uziyeli,
mbale wa atate wa Aroni, nanena nao, Senderani pafupi, nyamulani abale anu
muwacotse pakhomo pa malo opatulika kumka nao kunja kwa
cigono. 5Pamenepo anasendera pafupi, nawanyamula osawabvula maraya ao
a m'kati, kumka nao kunja kwa cigono, monga Mose adauza. 6Ndipo Mose
anati kwa Aroni, ndi kwa Eleazara ndi Itamara ana ace, Musawinda tsitsi,
musang'amba zobvala zanu; kuti mungafe, ndi kuti angakwiye iye ndi khamu
lonse; koma abale anu, mbumba yonse ya Israyeli, alire cifukwa ca motowu
Yehova anauyatsa. 7Ndipo musaturuka pakhomo pa cihema cokomanako, kuti
mungafe, pakuti mafuta odzoza a Yehova ali pa inu. Ndipo anacita monga
mwa mau a Mose.
8Ndipo Yehova ananena ndi Aroni, nati, 9Usamamwa vinyo, kapena
coledzeretsa, iwe ndi ana ako omwe, m'mene mulowa m'cihema cokomanako,
kuti mungafe; likhale lemba losatha mwa mibadwo yanu; 10ndi kuti
musiyanitse pakati pa copatulika ndi cosapatulika, ndi pakati pa codetsa ndi
coyera; 11ndi kuti muphunzitse ana a Israyeli malemba onse amene Yehova
analankhula nao ndi dzanja la Mose.
12Ndipo Mose ananena ndi Aroni, ndi Eleazara ndi Itamara, ana ace otsala,
Tengani nsembe yaufa yotsalira ku nsembe zamoto za Yehova, ndi kuidya
yopanda cotupitsa pafupi pa guwa la nsembe; pakuti ndiyo
yopatulikitsa; 13ndipo muziidyera kumalo kopatulika, popeza ndiyo gawo lako,
ndi gawo la ana ako, locokera ku nsembe zamoto za Yehova; pakuti anandiuza
cotero. 14Ndi nganga yoweyula ndi mwendo wokweza mudyere izi pamalo
poyera; iwe ndi ana ako amuna, ndi ana ako akazi omwe, popeza zapatsidwa
gawo lako ndi gawo la ana ako amuna, zocokera ku nsembe zoyamika za ana
a Israyeli. 15Mwendo wokweza, ndi nganga yoweyula adze nazo pamodzi ndi
nsembe zamoto zamafuta, aziweyule nsembe yoweyula pamaso pa Yehova;
ndipo zikhale zako ndi za ana ako amuna, mwa lemba losatha; monga Yehova
anauza.
16Ndipo Mose anafunafuna mbuzi ya nsembe yaucimo, ndipo, taonani,
adaitentha. 17Ndipo anapsa mtima pa Eleazara ndi Itamara, ana otsalawo a
Aroni, nati, Mwalekeranji kudya nsembe yaucimo m'malo opatulika, pakuti
ndiyo yopatulikitsa, ndipo iye anakupatsani iyo, kucotsera nayo mphulupulu
ya khamulo, kuwacitira cowatetezera pamaso pa Yehova? 18Taonani,
sanalowa nao mwazi wace m'malo opatulika m'katimo; mukadaidyera ndithu
m'malo opatulika, monga ndinakuuzani. 19Ndipo Aroni analankhula ndi Mose,
nati, Taonani, lero abwera nayo nsembe yao yaucimo ndi nsembe yao
yopsereza pamaso pa Yehova; ndipo zandigwera zotere; ndikadadya nsembe
yaucimo lero, kukadakomera kodi pamaso pa Yehova? 20Pamene Mose
adamva ici cidamkomera pamaso pace.

Za nyama zodyeka ndi zosadyeka ndi zakufa zodetsa munthu

1Ndipo Yehova ananena ndi Mose ndi Aroni, nati nao, 2Nenani ndi ana a
Israyeli, ndi kuti, Izi ndi zamoyo zimene muyenera kumadya mwa nyama
zonse ziri pa dziko lapansi. 3Nyama iri yonse yogawanika ciboda, nikhala
yogawanikadi ciboda, ndi yobzikula, imeneyo muyenera kudya. 4Koma izi
zokha simuyenera kuzidya mwa zobzikulazo, kapena zogawanika ciboda;
ngamila, angakhale abzikula, koma yosagawanika ciboda, muziiyesa
yodetsedwa. 5Ndi mbira, ingakhale ibzikula koma yosagawanika ciboda,
muiyese yodetsedwa. 6Ndi kalulu, popeza abzikula koma wosagawanika
ciboda, mumuyese wodetsedwa. 7Ndi nkhumba, popeza igawanika ciboda,
nikhala yogawanikadi ciboda, koma yosabzikula, muiyese
yodetsedwa. 8Nyama yace musamaidya, mitembo yace musamaikhudza;
muziyese zodetsedwa.
9Mwa zonse ziri m'madzi muyenera kumadya izi: ziri zonse ziti nazo zipsepse
ndi mamba m'madzi, m'nyanja, ndi m'mitsinje, zimenezo muyenera
kumadya. 10Koma ziti zonse ziribe zipsepse ndi mamba m'nyanja, ndi
m'mitsinje, mwa zonse zokwawa za m'madzi, ndi mwa zamoyo zonse ziri
m'madzi, muziziyesa zonyansa; 11inde muziyese zonyansa; musamadya
nyama zao; mitembo yao zikunyansireni. 12Ziri zonse zopanda zipsepse
kapena mamba m'madzimo muziyese zonyansa.
13Ndipo mwa mbalame muziziyesa zonyansa izi; siziyenera kuzidya, zonyansa
ndi izi: mphungu, ndi nkhwazi, ndi cikambi; 14ndi muimba, ndi mphamba mwa
mtundu wace; 15kungubwi mwa mtundu wace; 16ndi nthiwatiwa, ndi cipudo,
ndi kakoa, ndi kabawi mwa mtundu wace; 17ndi nkhutunkhutu ndi
nswankhono ndi mancici; 18tsekwe, bvuwo, ndi dembu; 19indwa, ndi cimeza
monga mwa mtundu wace, ndi sadzu, ndi mleme.
20Zokwawa zonse zakuuluka zokhala ndi miyendo inai, muziyesa izi
zonyansa, 21Koma muyenera kudya izi mwa zokwawa zonse zakuuluka,
zokhala ndi miyendo inai, zokhala ndi miyendo pa mapazi ao, ya kuthumpha
nayo pansi; mwa zimenezi muyenera kudya izi: 22dzombe mwa mtundu wace,
ndi cirimamine mwa mitundu yace, ndi njenjete mwa mtundu wace ndi
tsokonombwe mwa mitundu yace. 23Koma zokwawa zonse zakuuluka, za
miyendo inai, muziyese zonyansa.
24Ndipo izi zikudetsani: ali yense akhudza mtembo wace adzakhala
wodetsedwa kufikira madzulo; 25ndipo ali yense akanyamulako nyama ya
mtembo wace azitsuka zobvala zace, nadzakhala wodetsedwa kufikira
madzulo. 26Nyama iri yonse yakugawanika ciboda, koma yosagawanikitsa, ndi
yosabzikula, muiyese yodetsa; ali yense wakuikhudza adzakhala
wodetsedwa. 27Ndipo iri yonse iyenda yopanda ciboda mwa zamoyo zonse za
miyendo inai, muiyese yodetsedwa; ali yense wokhudza mtembo wace
adzakhala wodetsedwa kufikira madzulo. 28Ndipo iye amene akanyamula
mtembo wace atsuke zobvala zace, nadzakhala wodetsedwa kufikira madzulo;
muziyese izi zodetsa.
29Ndipo izi ndi zimene muziziyesa zodetsedwa mwa zinthu zokwawa
zakukwawa pansi; likongwe, ndi mbewa, ndi msambulu mwa mtundu
wace; 30ndi gondwa, ndi mng'anzi, ndi buluzi, ndi dududu, ndi mfuko. 31Izi ndi
zimene muziyese zodetsa, mwa zonse zakukwawa; ali yense azikhudza zitafa,
adzakhala wodetsedwa kufikira madzulo. 32Ndipo ciri conse cakufa ca izi
cikagwera kanthu, kanthuka kadzakhala kodetsedwa; ngakhale cipangizo
camtengo, kapena cobvala, kapena cikopa kapena thumba, cipangizo ciri
conse cimene agwira naco nchito, acibviike m'madzi, ndipo cidzakhala

codetsedwa kufikira madzulo; pamenepo cidzakhala coyera. 33Ndipo ciri conse ca izi cikagwa m'cotengera ciri conse cadothi, cinthu cokhala m'mwemo cidetsedwa, ndi cotengeraco muciswe. 34Cakudya ciri conse cokhala m'mwemo, cokonzeka ndi madzi, cidzakhala codetsedwa; ndi cakumwa ciri conse m'cotengera cotere cidzakhala codetsedwa. 35Ndipo kanthu ka mtembo wace kakagwa pa zinthu ziri zonse zidzakhala zodetsedwa; ngakhale mcembo kapena mphika wobvundikika, aziswe; zodetsa izi, muziyese zodetsedwa. 36Koma kasupe kapena citsime muli madzi, zidzakhala zoyera; koma iye amene akhudza mitembo yao adzadetsedwa. 37Ndipo kanthu ka mtembo wace kakagwa pa mbeu yofesa, ikati ifesedwe, idzakhala yoyera. 38Koma akathira madzi pa mbeuyi, ndi kanthu ka mtembo wace kakagwapo, muiyese yodetsedwa.
39Ndipo ikafa nyama yakudya, iye amene akhudza mtembo wace adzakhala wodetsedwa kufikira madzulo. 40Ndipo iye wakudya kanthu ka mtembo wace azitsuka zobvala zace, nadzakhala wodetsedwa kufikira madzulo; iyenso wakunyamula mtembo wace atsuke zobvala zace, nadzakhala wodetsedwa kufikira madzulo.
41Ndipozokwawazonsezakukwawa pa dziko lapansi zikhale zonyansa; musamazidya. 42Zonse zoyenda cafufumimba, ndi zonse za miyendo inai, kapena zonse zokhala nayo miyendo yambiri ndi zokwawa zonse zakukwawa pansi, musamazidya; popeza ndizo zonyansa. 43Musamadzinyansitsa ndi cokwawa ciri conse cakukwawa, musamadzidetsa nazo, kuti mukadziipse nazo. 44Pakuti Ine ndine Yehova Mulungu wanu; potero dzipatuleni, ndipo muzikhala oyera; pakuti Ine ndine woyera; ndipo musamadziipsa ndi cokwawa ciri conse cakukwawa pansi. 45Pakuti Ine ndine Yehova amene ndinakukwezani kukuturutsani m'dziko la Aigupto, ndikhale Mulungu wanu; cifukwa cace mukhale oyera, popeza ine ndine woyera.
46Ici ndi cilamulo ca nyama, ndi ca mbalame, ndi ca zamoyo zonse zakuyenda m'madzi, ndi ca zamoyo zonse zakukwawa pansi; 47kusiyanitsa pakati zodetsa ndi zoyera, ndi pakati pa zamoyo zakudya ndi zamoyo zosadya.

Za kuyeretsedwa kwa mkazi

1Ndipo Yehova ananena ndi Mose, nati, 2Nena ndi ana a Israyeli, ndi kuti, Akaima mkazi, nakabala mwana wamwamuna, adzakhala wodetsedwa masiku asanu ndi awiri; monga masiku ace akukhala padera, podwala iye, adzakhalawodetsedwa. 3Ndipo tsiku lacisanu ndi citatu adule khungu la mwanayo. 4Ndipo akhale m'mwazi wa kumyeretsa kwace masiku makumi atatu kudza atatu; asakhudze kanthu kopatulika, kapena kulowa m'malo opatulika, kufikira adakwanira masiku a kumyeretsa kwace. 5Koma akabala mwana wamkazi, akhale wodetsedwa masabata awiri, monga umo amakhala padera; ndipo adzakhala m'mwazi wa kumyeretsa kwace masiku makumi asanu ndi limodzi kudza asanu ndi limodzi. 6Ndipo atakwanira masiku a kumyeretsa kwace pa mwana wamwamuna, kapena mwana wamkazi, adze naye mwana wa nkhosa wa caka cimodzi ikhale nsembe yopsereza, ndi bunda, kapena njiwa zikhale nsembe yaucimo, ku khomo la cihema cokomanako, kwa wansembe; 7ndipo iye abwere nayo pamaso pa Yehova, namcitire comtetezera mkaziyo, ndipo adzakhala woyeretsedwa wocira kukha mwazi kwace. 8Ici ndi cilamulo ca kwa iye wakubala, kapena mwana wamwamuna kapena wamkazi. Ndipo cuma cace cikapanda kufikira nkhosa, atenge njiwa ziwiri kapena maunda awiri; lina likhale nsembe yopsereza, ndi lina nsembe yaucimo; ndi wansembe amcitire comtetezera, ndipo adzakhalawoyera.

Malamulo a pa nthenda yakhate

1Ndipo Yehova ananena ndi Mose ndi Aroni, nati, 2Ngati munthu ali naco
cotupa, kapena nkhanambo, kapena cikanga pa khungu la thupi lace, ndipo
isandulika nthenda yakhate pa khungu la thupi lace, azifika kwa Aroni
wansembe, kapena kwa mmodzi wa ana ace ansembe; 3ndipo wansembe
aione nthenda pa khungu la thupi; ndipo ngati tsitsi la panthenda lasanduka la
mbu, ndi nthenda ikaoneka yapitirira khungu la thupi lace, ndiyo nthenda
yakhate; ndipo wansembe amuone, namuche wodetsedwa. 4Koma ngati
cikanga cikhala cotuwa pa khungu la thupi lace, ndipo cikaoneka cosapitirira
khungu, ndi tsitsi lace losasanduka loyera, pamenepo wansembe
ambindikiritse wanthendayo masiku asanu ndi awiri; 5ndipo wansembe
amuonenso tsiku lacisanu ndi ciwiri; ndipo taonani, monga momwe apenyera
iye, nthenda yaima, nthenda siinapitirira pakhungu, pamenepo wansembe
ambindikiritsenso masiku asanu ndi awiri ena; 6ndipo wansembe amuonenso
tsikulacisanu ndi ciwiri, ndipo taonani, nthenda yazimba yosapitirira khungu
nthendayi, pamenepo wansembe amuche iye woyera, ndiyo nkhanambo
cabe; ndipo atsuke zobvala zace, ndiye woyera; 7koma nkhanambo ikapitirira
khungu, atadzionetsakwa wansembe kuti achedwe woyera, adzionetsenso
kwa wansembe; 8ndipo wansembe aone, ndipo taonani, ngati nkhanambo
yapitirira khungu, wansembe amuche wodetsedwa, ndilo khate.
9Pamene nthenda yakhate iri mwa munthu, azimfikitsa kwa
wansembe; 10ndipo wansembe aone, ndipo taonani, ngati pali cotupa coyera
pakhungu, ndipo casanduliza tsitsi likhale loyera, ndipo pacotupa pali mnofu
wofiira, 11ndilo khate lakale pa khungu la thupi lace, ndipo wansembe
amuche wodetsedwa; asambindikiritse popeza ali wodetsedwa. 12Ndipo ngati
khate libukabuka pakhungu, ndi khate lakuta khungu lonse la wanthendayo
kuyambira mutu wace kufikira mapazi ace, monga momwe apenyera
wansembe; 13pamenepo wansembe aone, ndipo taonani, ngati khate lakuta
thupi lace, amuche woyera wanthendayo; patuwa ponsepo; ndiye
woyera. 14Koma tsiku liri lonse ukaoneka pa iye mnofu wofiira, adzakhala
wodetsedwa, 15Ndipo wansembe aone mnofu wofiirawo, namuche
wodetsedwa; mnofu wofiira ndiwo wodetsa; ndilo khate. 16Kapena mnofu
wofiira ukasandukanso, nusandulika wotuwa, afike kwa wansembe, 17ndi
wansembe amuone, ndipo taonani, ngati nthenda yasandulika yotuwa,
wansembe amuche woyera wanthendayo; ndiye woyera.
18Ndipo pamene thupi liri ndi cironda pakhungu pace, ndipo capola, 19ndipo
padali cironda pali cotupa coyera, kapena cikanga cotuuluka, pamenepo
acionetse kwa wansembe; ndipo wansembe aone, 20ndipo taonani, ngati
cioneka cakumba kubzola khungu, ndipo tsitsi lace lisanduka lotuwa,
pamenepo wansembe amuche wodetsedwa; ndiyo nthenda yakhate yabuka
m'cirondamo. 21Koma wansembe akaciona, ndipo taonani, palibe tsitsi loyera
pamenepo, ndipo sicinakumba kubzola khungu, koma cazimba, pamenepo
wansembe ambindikiritse masiku asanu ndi awiri; 22ndipo ngati capitirira
khungu, wansembe amuche wodetsedwa; ndilo khate. 23Koma ngati cikanga
caima pomwepo, cosakula, ndico cipsera ca cironda; ndipo wansembe
amuche woyera.
24Kapena pamene thupi lidapsya ndi mota pakhungu pace, ndipo mnofu
wofiira wakupsyawo usanduka cikanga cotuuluka, kapena
cotuwa: 25pamenepo wansembe acione; ndipo taonani, ngati tsitsi la cikanga
lasanduka lotuwa, ndipo cioneka cakumba kubzola khungu; pamenepo ndilo
khate lobuka m'kupsyamo; ndipo wansembe azimucha wodetsedwa ndi

nthenda yakhate. 26Koma akaonapo wansembe, ndipo taonani, mulibe tsitsi loyera m'cikangamo, ndipo sicikumba kubzola khungu, koma cazimba; pamenepo wansembe ambindikiritse masiku asanu ndi awiri; 27ndipo wansembe amuone tsiku lacisanu ndi ciwiri; ngati cakula pakhungu, wansembe amuche wodetsedwa; ndiyo nthenda yakhate, 28Ndipo ngati cikanga ciima pomwepo, cosakula pakhungu koma cazimba; ndico cotupa ca kupsya; ndipo wansembe amuche woyera; pakuti ndico cipsera ca kupsya.
29Ndipo ngati mwamuna kapena mkazi ali ndi nthenda pamutu kapena pandebvu, 30wansembe aziona nthenda; ndipo taonani, ngati ioneka yokumba kubzola khungu, ndipo pali tsitsi loyezuka lotetemera; pamenepo wansembe amuche wodetsedwa; ndiyo mfundu, ndilo khate la mutu kapena ndebvu. 31Ndipo wansembe akaona nthenda yamfundu, ndipo taonani, ioneka yosakumba kubzola khungu, ndipo palibe tsitsi lakuda pamenepo, wansembe ambindikiritse iye ali ndi mfundu masiku asanu ndi awiri; 32ndipo tsiku lacisanu ndi ciwiri wansembe aone nthendayi; ndipo taonani, ngati mfundu njosakula, ndipo mulibe tsitsi loyezuka, ndipo mfundu ikaoneka yosakumba kubzola khungu, 33pamenepo azimeta, koma osameta pamfundu; ndipo wansembe ambindikiritse iye wamfundu masiku asanu ndi awiri ena; 34ndipo tsiku lacisanu ndi ciwiri aone mfunduyo; ndipo taonani, ngati mfundu njosakula pakhungu, ndipo ioneka yosakula kubzola khungu, wansembe amuche woyera, ndipo iye atsuke zobvala zace, nakhala woyera. 35Koma ngati mfundu ikula pakhungu atachedwa woyera; 36pamenepo wansembe amuone, ndipo taonani, ngati mfundu yakula pakhungu, wansembe asafunefune tsitsi loyezuka, ndiye wodetsedwa. 37Koma monga momwe apenyera iye, ngati mfundu yaima pomwe, ndipo pamera tsitsi lakuda, mfundu yapola, ndiye woyera, ndipo wansembe amuche woyera.
38Ndipo ngati mwamuna kapena mkazi ali ndi zikanga pa khungu la thupi lace, zikanga zoyerayera; 39wansembe aziona; ndipo taonani ngati zikanga ziri pa khungu la thupi lao zikhala zotuwatuwa; ndilo thuza labuka pakhungu; ndiye woyera. 40Ndipo ngati tsitsi la munthu lathothoka, ndiye wadazi; koma woyera. 41Ndipo ngati tsitsi lathothoka pamphumi pace ndiye wa masweswe, koma woyera. 42Koma ngati pali nthenda yotuuluka pakati pa dazi lace la pamutu, kapena la pamphumi, ndipo khate lirikubuka pakati pa dazi lace la pamutu, kapena la pamphumi. 43Pamenepo wansembe azimuona, ndipo taonani, ngati cotupa cace ca nthenda ciri cotuuluka pa dazi la pa mutu wace, kapena la pamphumi pace, monga maonekedwe a khate pa khungu la thupi; 44ndiye wakhate, ndiye wodetsedwa; wansembe amuchetu wodetsedwa; nthenda yace iri pamutu pace.
45Ndipo azing'amba zobvala zace za wakhate ali ndi nthendayo, ndi tsitsi la pamutu pace lizikhala lomasuka, naphimbe iye mlomo wace wa m'mwamba, napfuule, Wodetsedwa, wodetsedwa! 46Masiku onse nthenda ikali pa iye azikhala wodetsedwa; ali wodetsedwa, agone pa yekha pokhala pace pakhale kunja kwa cigono.
47Ndiponso ngati nthenda yakhate iri pa cobvala caubweya, kapena cathonje; 48ngakhale iri pamuyaro, kapena pamtsendero, cathonje, kapena caubweya, ngakhale iri pa cikopa, kapena pa cinthu ciri conse copanga ndi cikopa; 49ngati nthenda iri yobiriwira, kapena yofiira pacobvala, kapena pacikopa, kapena pamuyaro, kapena pamtsendero, kapena pa cinthu ciri conse copangika ndi cikopa, ndiyo nthenda yakhate; aziionetsa kwa wansembe; 50ndipo wansembe aone nthendayo, nabindikiritse ciija ca nthenda masiku asanu ndi awiri; 51naone nthenda tsiku lacisanu ndi ciwiri; ngati nthenda yakula pacobvala, ngakhale pamuyaro, kapena pamtsendero,

kapena pacikopa, ziri zonse zanchito zopangika ndi cikopa; nthendayo ndiyo khate lofukuta; ndico codetsedwa. 52Ndipo atenthe cobvalaco ngakhale muyaro wace, ngakhale mtsendero wace, caubweya kapena cathonje, kapena ciri conse cacikopa ciri ndi khate, ndilo khate lofetsa; acitenrhe ndi mote. 53Ndipo wansembe akaona, ndipo taonani, nthenda njosakula pacobvala, kapena pamuyaro, kapena pamtsendero, kapena pa cinthu ciri conse copangika ndi cikopa; 54pamenepo wansembe aziuza kuti atsuke cija pali khate, nacibindikiritse masiku asanu ndi awiri ena; 55ndipo wansembe aone nthenda ataitsuka, ndipo taonani, ngati nthendayi siinasandulika maonekedwe ace, yosakulanso nthenda, ndico codetsedwa; ucitenthe ndi moto; ndilo pfunka, kungakhale kuyera kwace kuli patsogolo kapena kumbuyo. 56Ndipo wansembe akaona, ndipo taonani, nthenda yazimba ataitsuka, pamenepo aikadzule pa cobvala, kapena cikopa, kapena muyaro, kapena mtsendero; 57ndipo ikaonekabe pacobvala, ngakhale pamuyaro, kapena pamtsendero, kapena pa cinthu ciri conse copangika ndi cikopa, irikubukanso; ucitenthe ndi moto cija canthenda. 58Ndipo ukatsuka cobvalaco, kapena muyaro, kapena mtsendero, kapena cinthu ciri conse copangika ndi cikopa, ngati nthenda yalekapo pa cimeneco, acitsukenso kawiri, pamenepo ciri coyera. 59Ici ndi cilamulo ca nthenda yakhate iri pa cobvala caubweya kapena cathonje, ngakhale pamuyare, kapena pamtsendero, kapena pa cinthu ciri conse copangika ndi cikopa; kucicha coyera kapena kucicha codetsa.

Malamulo a pa kumyeretsa wakhate

1Ndipo Yehova ananena ndi Mose nati, 2Cilamulo ca wakhate tsiku la
kumyeretsa kwace ndi ici: azidza naye kwa wansembe; 3ndipo wansembe
aturuke kumka kunja kwa cigono; ndipo wansembe aone, ndipo taonani, ngati
nthenda Yakhate yapola pa wakhateyo; 4pamenepo wansembe auze kuti
amtengere iye wakuti akonzedwe, mbalame ziwiri zoyera zamoyo, ndi mtengo
wamkungudza, ndi, ubweya wofiira, ndi hisope; 5ndipo wansembe auze kuti
aphe mbalame imodzi m'mbale yadothi pamwamba pa madzi
oyenda; 6natenge nbalame yamoyo, ndi mtengo wankungudza, ndi ubweya
wofiira, ndi hisope, nazibviike pamodzi ndi mbalame yamoyo m'mwazi wa
mbalame adaipha pamwamba pa madzi oyenda; 7nawaze kasanu ndi kawiri
iye amene akuti amyeretse khate lace, namuche woyera, nataye mbalame
yamoyo padambo poyera. 8Ndipo iye wakutiayeretsedwe atsuke zobvala zace,
namete tsitsi lace lonse, nasambe madzi, nakhale woyera; ndipo atatero
alowe kucigono, koma agone pa bwalo la hema wace masiku asanu ndi
awiri. 9Ndipo tsiku lacisanu ndi ciwiri kudzakhala kuti amete tsitsi lace lonse la
pamutu pace, ndi ndebvu zace, ndi nsidze zace, inde amete tsitsi lace lonse;
natsuke zobvala zace, nasambe thupi lace ndi madzi, nakhale
woyera. 10Ndipo tsiku lacisanu ndi citatu atenge ana a nkhosa awiri, amuna
opanda cirema, ndi mwana wa nkhosa mmodzi wamkazi wa caka cimodzi
wopanda cirema, ndi atatu a magawo khumi a ufa wosalala ukhale nsembe
yaufa, wosanganiza ndi mafuta, ndi muyeso umodzi wa mafuta. 11Ndipo
wansembe amene amyeretsayo, amuike munthu uja wakuti ayeretsedwe, ndi
zinthu zija, pamaso pa Yehova, pa khomo la cihema cokomanako; 12ndipo
wansembe atenge mwana wa nkhosa mmodzi wamwamuna, nabwere naye
akhale nsembe yoparamula, pamodzi ndi muyeso uja wa mafuta, naziweyule
nsembe yoweyula pamaso pa Yehova. 13Ndipo akaphere mwana wa nkhosa
wamwamuna paja amapherapo nsembe yaucimo, ndi nsembe yopsereza, pa
malo popatulika; pakuti monga nsembe yaucimo momwemo nsembe
yoparamula, nja wansembe; ndiyo yopatulikitsa. 14Ndipo wansembe atengeko
mwazi wa nsembe yoparamula, ndipo wansembe aupake pa ndewerere ya
khutu la ku dzanja lamanja la iye wakuti ayeretsedwe, ndi pa cala cacikuru ca
dzanja lace lamanja, ndi pa cala cacikuru ca phazi lace la ku dzanja
lamanja; 15ndipo wansembe atengeko muyeso wa mafuta, nawathire pa
cikhato ca dzanja lace lamanzere la iye mwini; 16ndipo wansembe abviike
cala cace ca dzanja lace lamanja ca iye mwini m'mafuta ali m'dzanja lace
lamanzere, nawaze mafuta kasanu ndi kawiri ndi cala cace pamaso pa
Yehova; 17ndipo wansembe apakeko mafuta okh a ria m'dzanja lace pa
ndewerere ya khutu la ku dzanja lamanja la iye wakuti ayeretsedwe, ndi pa
cala cacikuru ca dzanja lace lamanja, ndi pa cala cacikuru ca phazi lace la ku
dzanja lamanja, pa mwazi wa nsembe yoparamula; 18natsitsitize mafuta
otsala m'dzanja lace la wansembe, pamutu pa iye wakuti ayeretsedwe; ndipo
wansembe amcitire comtetezers pamaso pa Yehova. 19Ndipo wansembe
apereke nsembe yaucimo, namcitire comtetezera amene akuti ayeretsedwe,
cifukwa ca kudetsedwa kwace; ndipo atatero aphe nsembe
yopsereza; 20ndipo wansembe atenthe nsembe yopsereza, ndi nsembe yaufa
pa guwa la nsembe; ndipo wansembe amcitire comtetezera, ndipo adzakhala
iye woyera.
21Ndipo akakhala waumphawi cosafikana cuma cace azitenga mwana wa
nkhosa mmodzi wamwamuna akhale nsembe yoparamula, aiweyule kumcitira
comtetezera, ndi limodzi la magawo khumi la efa la ufa wosalala,

wosanganiza ndi mafuta, ukhale nsembe yaufa, ndi muyeso umodzi wa mafuta; 22ndi njiwa ziwiri, kapena maunda awiri, monga akhoza kufikana; limodzi likhale la nsembe yaucimo, ndi linzace la nsembe yopsereza. 23Ndipo tsiku lacisanu ndi citatu abwere nao kwa wansembe, ku khomo la cihema cokomanako, pamaso pa Yehova. 24Ndipo wansembe atenge mwana wa nkhosa wa nsembe yoparamula, ndi muyeso wa mafuta, ndipo wansembe aziweyule nsembe yoweyula pamaso pa Yehova; 25naphe mwana wa nkhosa wa nsembe yoparamula, ndipo wansembe atengeko mwazi wa nsembe yoparamula, naupake pa ndewerere ya khutu la ku dzanja lamanja la iye akuti ayeretsedwe, ndi pa cala cacikuru ca dzanja lace lamanja, ndi pa cala cacikuru ca phazi lace la ku dzanja lamanja; 26ndipo wansembe athireko mafuta aja m'cikhato cace camanzere ca iye mwini; 27ndipo wansembe awazeko mafuta aja ali m'dzanja lace lamanzere ndi cala cace ca dzanja lamanja, kasanu ndi kawiri pamaso pa Yehova; 28ndipo wansembe apakeko mafuta aja ali m'dzanja lace pa ndewerere ya khutu la ku dzanja lamanja la iye wakuti ayeretsedwe, ndi pa cala cacikuru ca: dzanja lace lamanja, ndi pa cala cacikuru ca phazi lace la ku dzanja lamanja, pa malo paja pali mwazi wa usembe yoparamula; 29ndipo mafuta otsala m'dzanja la wansembe atsitsitize pa mutu wa iye wakuti ayeretsedwe, kumcitira comtetezera pamaso pa Yehova. 30Ndipo iye apereke imodzi ya njiwazo, kapena limodzi la maunda, monga akhoza kufikana nazo, limodzi la nsembe yaucimo, ndi tina la nsembe yopsereza, pamodzi ndi nsembe yaufa; 31ndipo wansembe amcitire comtetezera pamaso pa Yehova. 32Ici ndi cilamulo ca iye ali ndi nthenda yakhate, wosakhoza kufikana nazo zofunika pomyeretsa pace.
33Ndipo Yehova ananena ndi Mose ndi Aroni, nati, 34Mutakafika m'dziko la Kanani, limene ndikupatsani likhale lanu lanu, ndipo ndikaika nthenda yakhate m'nyumba ya dziko lanu lanu; 35pamenepo mwini nyumbayo adzauze wansembe, kuti, Ndiyesa muli ngati nthenda m'nyumba. 36Ndipo wansembe aziuza kuti aturutse zonse za m'nyumba, asanalowe kudzaona nthendayi, zinthu zonse ziri m'nyumba zingakhale zodetsedwa; ndipo atatero wansembe alowe kukaona nyumbayi; 37naone nthendayo, ndipo taonani, nthenda ikakhala yosumbudzuka m'makoma a nyumba yobiriwira kapena yofiira, ndipo maonekedwe ace yakumba kubzola khoma; 38pamenepo wansembe azituruka ku khomo la nyumba, natseke nyumbayo masiku asanu ndi awiri; 39ndipo wansembe abwerenso tsiku lacisanu ndi ciwiri, naonenso, ndipo taonani, ngati nthenda yakula m'makoma a nyumba; 40pamenepo wansembe auze kuti agumule miyalayi pali nthenda, naitayire ku malo akuda kunja kwa mudzi; 41napalitse nyumba m'kati monsemo, natayire ku malo akuda kunja kwa mudzi dothi adapalako; 42natenge miyala yina, naikhazike m'male mwa miyala ija; natenge dothi tina, namatenso nyumbayo. 43Ndipo ikabweranso nthenda, nibukanso m'nyumba atagumula miyala, ndipo atapala m'nyumba namatanso; 44pamenepo wansembe alowe naonemo, ndipo taonani, ngati nthenda yakula m'nyumba, ndiyo khate lonyeka m'nyumba; ndiyo yodetsedwa. 45Ndipo apasule nyumbayo, miyala yace, ndi mitengo yace, ndi dothi lace lonse kumudzi kuzitaya ku malo akuda. 46Ndiponso iye wakulowa m'nyumba masiku ace iriyotsekedwa, adzakhala wodetsedwa kufikira madzulo. 47Ndipo iye wakugona m'nyumbayo atsuke zobvala zace; ndi iye wakudya m'nyumbayo atsuke zobvala zace. 48Ndipo wansembe akalowa, nakaona, ndipo taonani, nthenda siinakula m'nyumba, ataimata nyumba; wansembe aiche nyumbayo yoyera, popeza nthenda yaleka. 49Pamenepo atenge mbalame ziwiri, ndi mtengo wamkungudza, ndi ubweya wofiira, ndi hisope, kuti ayeretse nazo nyumbayo; 50naphe mbalame imodzi m'mbale

yadothi, pamwamba pa madzi oyenda; 51natenge mtengo wamkungudza ndi
hisope, ndi ubweya wofiira, ndi mbalame yamoyo, nazibviike m'mwazi wa
mbalame yakuphayo, ndi m'madzi oyenda, nawaze kasanu ndi kawiri
m'nyumba; 52nayeretsenyumbandi mwazi wa mbalame, ndi madzi oyenda,
ndi mbalame yamoyo, ndi mtengo wamkungudza, ndi hisope, ndi ubweya
wofiira. 53Koma ataye mbalame yamoyo kunja kwa mudzi kuthengo koyera;
motero aicitire coitetezera nyumbayo; ndipo idzakhala yoyera.
54Ici ndi cilamulo ca nthenda iri yonse yakhate, ndi yamfundu; 55ndi ya khate
la cobvala, ndi la nyumba; 56ndi yacotupa, ndi yankhanambo, ndi
yacikanga; 57kulangiza tsiku loti cikhala codetsa, ndi tsiku loti cikhala coyera;
ici ndi cilamulo ca khate.

Ndipo Yehova ananena ndi

1Mose ndi Aroni, nati, 2Nenani nao ana a Israyeli, nimuti nao, Pamene mwamuna ali yense ali ndi nthenda yakukha m'thupi mwace, akhale wodetsedwa, cifukwaca kukha kwace. 3Ndipo kudetsedwa kwa kukha kwace ndiko: ngakhale cakukhaco cituruka m'thupi mwace, ngakhale caleka m'thupi mwace, ndiko kumdetsa kwace. 4Kama ali yense agonapo wakukhayo ali wodetsedwa; ndi cinthu ciri conse acikhalira ciri codetsedwa. 5Ndipo munthu ali yense wakukhudza kama wace azitsuka zobvala zace, nasambe m'madzi, nadzakhala wodetsedwa kufikira madzulo, 6Ndipo iye wakukhalira cinthu ciri conse adacikhalira wakukhayo atsuke zobvala zace, nasambe m'madzi, nadzakhala wodetsedwa kufikira madzulo. 7Ndipo iye wakukhudza thupi la uyo wakukhayo atsuke zobvala zace, nasambe m'madzi, nadzakhala wodetsedwa kufikira madzulo. 8Ndipo wakukhayo akalabvulira wina woyera; pamenepo atsuke zobvala zace, nasambe m'madzi, nadzakhala wodetsedwa kufikira madzulo. 9Ndipo mbereko iri yonse akwerapo wakukhayo iri yodetsedwa. 10Ndipo munthu ali yense akakhudza kanthu kali konse kadali pansi pace adzakhala wodetsedwa kufikira madzulo; ndipo iye wakunyamula zimenezo atsuke zobvala zace, nasambe m'madzi, nadzakhala wodetsedwa kufikira madzulo. 11Ndipo munthu ali yense wakukhayo akamkhudza, osasambatu m'manja m'madzi, atsuke zobvala zace, nasambe m'madzi, nadzakhala wodetsedwa kufikira madzulo. 12Ndipo zotengera zadothi wazikhudza wakukhayo, aziphwanye; ndi zamtengo, azitsuke ndi madzi. 13Ndipo wakukhayo atayeretsedwa ku kukha kwace, adziwerengere masiku asanu ndi awiri akhale a kuyeretsa kwace, natsuke zobvala zace; nasambe thupi lace ndi madzi oyenda, nadzakhala woyera. 14Ndipo tsiku lacisanu ndi citatu atenge njiwa ziwiri, kapena maunda awiri, nafike pamaso pa Yehova pa khomo la cihema cokomanako, nazipereke kwa wansembe; 15ndipo wansembe azipereke izo, imodzi ikhale nsembe yaucimo, ndi yina nsembe yopsereza; ndipo wansembe amcitire comtetezera pamaso pa Yehova cifukwa ca kukha kwace.

16Ndipo munthu ali yense akagona uipa, azisamba thupi lace lonse ndi madzi, nadzakhala wodetsedwa kufikira madzulo. 17Ndipo cobvala ciri conse, ndi cikopa ciri conse, anagona uipa pamenepo azitsuke ndi madzi, nizidzakhala zodetsedwa kufikira madzulo. 18Mkazi yemwe, mwamuna atagona naye, onse awiri asambe ndi madzi, nadzakhala odetsedwa kufikira madzulo.

19Ndipo ngati mkazi ali ndi nthenda yakukha, ndi kukha kwace nkwa mwazi m'thupi mwace, akhale padera masiku asanu ndi awiri; ndipo ali yense amkhudza adzakhala wodetsedwa kufikira madzulo. 20Ndipo cinthu ciri conse agonapo pokhala ali padera ncodetsedwa; ndi cinthu ciri conse akhalapo ncodetsa. 21Ndipo ali yense akhudza kama wace azitsuka zobvala zace, nasambe m'madzi, nadzakhala wodetsedwa kufikira madzulo. 22Ndipo ali yense akhudza cinthu ciri conse akhalapo iye, atsuke zobvala zace, nasambe m'madzi, nadzakhala wodetsedwa kufikira madzulo. 23Ndipo cikakhala pakama, kapena pa cinthu ciri conse akhalapo iye, atacikhudza, adzakhala wodetsedwa kufikira madzulo. 24Ndipo ngati mwamuna ali yense agona naye, ndi kudetsa kwace kukhala pa iye, adzakhala wodetsedwa masiku asanu ndi awiri; ndipo kama ali yense agonapo ali wodetsedwa.

25Ndipo mkazi akakhala ndi kukha mwazi masiku ambiri, osati masiku a kuoloka kwace, kapena akamakha kupitirira nthawi ya kuoloka kwace; masiku onse cirinkukha comdetsa cace, adzakhala wodetsedwa, monga masiku a kuoloka kwace. 26Kama ali yense agonapo masiku a kukha kwace akhale

ngati kama wa kuoloka kwace; ndi cinthu ciri conse akhalapo ciri codetsedwa, ngati kudetsa kwa kuoloka kwace. 27Ndipo munthu ali yense akakhudza zimenezi adzakhala wodetsedwa, natsuke zobvala zace, nasambe m'madzi, nadzakhala wodetsedwa kufikira madzulo. 28Koma akayeretsedwa kukha kwace, adziwerengere masiku asanu ndi awiri, ndipo atatero adzakhala woyeretsedwa. 29Ndipo tsiku lacisanu ndi citatu atenge njiwa ziwiri, kapena maunda awiri, nafike nazo kwa wansembe ku khomo la cihema cokomanako. 30Ndipo wansembe apereke limodzi likhale nsembe yaucimo, ndi linalo likhale nsembe yopsereza; ndipo wansembe amcitire comtetezera pamaso pa Yehova cifukwa ca kukha kwace komdetsa.
31Motero muzipatula ana a Israyeli kwa kudetsedwa kwao; angafe m'kudetsedwa kwao, pamene adetsa kacisi wanga ali pakati pao.
32Ici ndi cilamulo ca wakukha, ndi ca iye wakugona uipa, kuti kumkhalitse wodetsedwa; 33ndi ca mkazi alinkudwala ndi kudetsedwa kwace, ndi ca iye alikukha kapena mwamuna, kapena mkazi, ndi ca iye agona ndi mkazi wodetsedwa.

Za tsiku lotetezera caka ndi caka

1Ndipo Yehova ananena ndi Mose, atamwalira ana amuna awiri a Aroni, muja
anasendera pamaso pa Yehova, namwalira; 2ndipo Yehova anati kwa Mose,
Nena ndi Aroni mbale wako, kuti asalowe nthawi zonse m'malo opatulika
m'tseri mwa nsaru yocinga, pali cotetezerapo cokhala palikasa, kuti angafe;
popeza ndioneka mumtambo pacotetezerapo. 3Aroni azilowa pa bwalo la malo
opatulika nazozo: ng'ombe yamphongo ikhale ya nsembe yaucimo, ndi
nkhosa yamphongo ikhale ya nsembe yopsereza. 4Abvale maraya a m'kati a
bafuta wopatulika, nakhale nazo zobvala za kumiyendo pathupi pace,
nadzimangire m'cuuno ndi mpango wabafuta, nabvale nduwira yabafuta; izi
ndi zobvala zopatulika; potero asambe thupi lace ndi madzi, ndi kubvala
izi. 5Ndipo ku khama la ana a Israyeli atenge atonde awiri akhale a nsembe
yaucimo, ndi nkhosa yamphongo imodzi ikhale ya nsembe yopsereza. 6Ndipo
Aroni abwere nayo ng'ombe ya nsembe yaucimo, ndiyo yace yace, nacite
codzitetezera iye yekha, ndi mbumba yace. 7Ndipo atenge mbuzi ziwirizo
naziimike pamaso pa Yehova pakhomo pa cihema cokomanako. 8Ndipo
Aroniayesemaere pa mbuzi ziwirizo; maere amodzi kwa Yehova, ndi amodzi
kwa Azazeli. 9Ndipo Aroni abwere nayo mbuzi imene adaigwera maere a
Yehova, naiyese nsembe yaucimo. 10Koma mbuzi imene adaigwera maere a
Azazeli, aiike yamoyo pamaso pa Yehova, kuti acite nayo cotetezera,
kuitumiza kucipululu ikhale ya Azazeli. 11Ndipo Aroni abwere nayo ng'ombe ya
nsembe yaucimo, ndiyo yace yace, nadzitetezere iye yekha, ndi mbumba
yace, ndi kupha ng'ombe ya nsembe yaucimo ndiyo yace yace; 12natenge
mbale ya zofukiza yodzala ndi makara amoto, kuwacotsa pa guwa la nsembe,
pamaso pa Yehova, ndi manja ace odzala ndi cofukiza copera ca pfungo
lokoma, nalowe nayo m'tseri mwa nsaru yocinga; 13naike cofukizaco pamoto
pamaso pa Yehova, kuti mtambo wa cofukiza ciphimbe cotetezerapo cokhala
pamboni, kuti angafe. 14Ndipo atengeko mwazi wa ng'ombeyo, ndi kuuwaza
ndi cala cace pacotetezerapo, mbali ya kum'mawa; nawaze mwazi ndi cala
cace cakuno ca cotetezerapo kasanu ndi kawiri. 15Pamenepo aiphe mbuzi ya
nsembe yaucimo, ndiyo yophera anthu, nalowe nao mwazi wace m'tseri mwa
nsaru yocinga, nacite nao mwazi wace monga umo anacitira ndi mwazi wa
ng'ombe, nauwaze pacotetezerapo ndi cakuno ca cotetezerapo; 16nacitire
cotetezera malo opatulika, cifukwa ca kudetsedwa kwa ana a Israyeli, ndi
cifukwa ca zolakwa zao, monga mwa zocimwa zao zonse; nacitire cihema
cokomanako momwemo, cakukhala nao pakati pa zodetsa zao. 17Ndipo
musakhale munthu m'cihema cokomanako pakulowa iye kucita cotetezera
m'malo opatulika, kufikira aturuka, atacita cotetezera yekha, ndi mbumba
yace, ndi msonkhano wonse wa Israyeli. 18Ndipo aturukire guwa la nsembe
lokhala pamaso pa Yehova ndi kulicitira cotetezera; natengeko mwazi wa
ng'ombeyo, ndi mwazi wa mbuziyo, ndi kuupaka pa nyanga za guwa la
nsembe pozungulira. 19Ndipo awazepo mwazi wina ndi cala cace kasanu ndi
katatu; ndi kuliyeretsa ndi kulipatula kulicotsera zodetsa za ana a
Israyeli. 20Ndipo atatha kucitira cotetezera malo opatulika, ndi cihema
cokomanako, ndi guwa la nsembe, abwere nayo mbuzi yamoyo; 21ndipo Aroni
aike manja ace onse awiri pamutu pa mbuzi yamoyo, ndi kubvomereza pa iyo
mphulupulu zonse za ana a Israyeli, ndi zolakwa zao zonse, monga mwa
zocimwa zao zonse; naike izi pamutu pa mbuziyo, ndi kuitumiza kucipululu ndi
dzanja la munthu wompangiratu, 22ndi mbuziyo isenze yokha mphulupulu
zonsezo kumka nazo ku dziko la pa lokha; ndipo azitaya mbuziyo
m'cipululu. 23Pamenepo Aroni alowe m'cihema cokomanako, nabvule zobvala

zabafuta zimene anazibvala polowa m'malo opatulika, nazisiye komweko. 24Ndipo asambe thupi lace ndi madzi kumalo kopatulika, nabvale zobvala zace, naturuke, napereke nsembe yopsereza yace, ndi nsembe yopsereza ya anthu, nacite codzitetezera yekha ndi anthu. 25Ndipo atenthe mafuta a nsembe yaucimo pa guwa la nsembe. 26Ndipo iye amene anacotsa mbuzi ipite kwa Azazeli atsuke zobvala zace, nasambe thupi lace ndi madzi, ndipo atatero alowenso kucigono. 27Koma ng'ombe ya nsembe yaucimo, ndi mbuzi ya nsembe yaucimo, zimene mwazi wao analowa nao kucita nao cotetezera m'malo opatulika, aturuke nazo kunja kwa cigono; natenthe ndi mota zikopa zao, ndi nyama zao, ndi cipwidza cao. 28Ndi iye amene anazitentha atsuke zobvala zace, nasambe thupi lace ndi madzi, ndipo atatero alowenso kucigono.
29Ndipo lizikhala kwa Inu lemba Ilosatha; mwezi wacisanu ndi ciwiri, tsiku lakhumi la mweziwo, muzidzicepetsa, osagwira Debito konse, kapena wa m'dziko, kapena mlendo wakukhala pakati panu; 30popeza tsikuli adzacitira inu cotetezera, kukuyeretsani; adzakuyeretsani, kukucotserani zoipa zanu zonse pamaso pa Yehova. 31Likhale kwa inu sabata lakupumula, kuti mudzicepetse; ndilo lemba losatha. 32Ndipo wansembe, amene anamdzoza ndi kumdzaza dzanja lace acite nchito ya nsembe m'malo mwa atate wace, acite cotetezera, atabvala zobvala zabafuta, zobvala zopatulikazo. 33Ndipo acite cotetezera malo opatulikatu, natetezere cihema cokomanako, ndi guwa la nsembe; momwemo atetezerenso ansembe, ndi anthu onse a msonkhanowo. 34Ndipo ici cikhale kwa inu lemba losatha, kucita cotetezera ana a Israyeli, cifukwa ca zocimwa zao zonse, kamodzi caka cimodzi. Ndipo anacita monga Yehova adauza Mose.

Popereka nsembe

1Ndipo Yehova ananena ndi Mose, nati, 2Nena ndi Aroni, ndi ana ace amuna, ndi ana a Israyeli onse, nuti nao, Ici ndi cimene Yehova wauza, ndi kuti, 3Munthu ali yense wa mbumba ya Israyeli akapha ng'ombe, kapena mwana wa nkhosa, kapena mbuzi, m'cigono, kapena akaipha kunja kwa cigono, 4osadza nayo ku khomo la cihema cokomanako, kuti aipereke copereka ca Yehova, ku bwalo la kacisi wa Yehova; azimuyesa munthuyu wocimwira mwazi, wakhetsa mwazi; ndipo amsadze munthuyo kumcotsa pakati pa anthu a mtundu wace; 5kotero kuti ana a Israyeli azidza nazo nsembe zao, zimene aziphera kuthengo koyera, kuti adze nazo kwa Yehova, ku khomo la cihema cokomanako, kwa wansembe, ndi kuziphera nsembe zoyamika za Yehova. 6Ndipo wansembeyo awaze mwaziwo pa guwa la nsembe la Yehova, pa khomo la cihema cokomanako, natenthe mafuta akhale pfungo lokoma lokwera kwa Yehova. 7Ndipo asamapheranso ziwanda nsembe zao, zimene azitsata ndi cigololo. Ili liwakhalire lemba losatha mwa mibadwo yao.

8Ndipo uzinena nao, Munthu ali yense wa mbumba ya Israyeli, kapena mlendo wakugonera pakati panu, amene apereka nsembe yopsereza kapena nsembe yophera, 9osadza nayo ku khomo la cihema cokomanako, kuiphera Yehova; amsadze munthuyu kumcotsa kwa anthu a mtundu wace.

Aletsedwa kudya mwazi

10Ndipo munthu ali yense wa mbumba ya Israyeli, kapena mlendo wogonera pakati panu, wakudya mwazi uli wonse; nkhope yanga idzatsutsana naye munthu wakudya mwaziyo, ndi kumsadza kumcotsa kwa anthu a mtundu wace. 11Pakuti moyo wa nyama ukhala m'mwazi; ndipo ndakupatsani uwu pa guwa la nsembe, ucite cotetezera moyo wanu; pakuti wocita cotetezera ndiwo mwazi, cifukwa ca moyo wace. 12Cifukwa cace ndinanena kwa ana a Israyeli, Asamadya mwazi mmodzi yense wa inu, kapena mlendo ali yense wakugoneramwa inu asamadya mwazi.

13Ndipo munthu ali yense wa ana a Israyeli, kapena mlendo wakugonera pakati pa inu, akasaka nyama kapena mbalame yakudya, nakaigwira; azikhetsa mwazi wace naufotsere ndi dothi. 14Pakuti ndiwo moyo wa: nyama zonse, mwazi wace ndiwo moyo wace; cifukwa cace ndinanena kwa ana a Israyeli, Musamadya mwazi wa nyama iri yonse; pakuti moyo wa nyama yonse ndi mwazi wace; ali yense akaudya adzasadzidwa. 15Ndipo ali yense wakudya yakufa yokha, kapena yojiwa kuthengo, ngakhale ndiye wa m'dziko kapena mlendo, azitsuka nsaru zace, nasambe ndi madzi, nadzakhala wodetsedwa kufikira madzulo; pamenepo adzakhala woyera. 16Koma akapanda kuzitsuka, kapena kusamba thupi lace, adzasenza mpholupulu yace.

Malamulo a pa ulemu

1Ndipo Yehova ananena ndi Mose, nati, 2Nena ndi ana a Israyeli, nuti nao, Ine ndine Yehova Molungu wanu. 3Musamacita monga mwa macitidwe a dziko la Aigupto muja munakhalamo; musamacita monga mwa macitidwe a dziko la Kanani kumene ndipita nanuko, nimusamayenda m'malemba ao. 4Muzicita maweruzo anga, ndi kusunga malemba anga, kumayenda m'mwemo; Ine ndine Yehova Mulungu wanu. 5Inde, muzisunga malemba anga, ndi maweruzo anga; amenewo munthu akawacita, adzakhala nao ndi moyo; Ine ndine Yehova.

6Asasendere mmodzi wa inu kwa mbale wacekumbvula; Ine ndine Yehova. 7Usamabvula atate wako, ndi mai wako; ndiye mai wako, usamambvula. 8Usamabvula mkazi wa atate wako; ndiye thupi la atate wako. 9Usamabvula mlongo wako, mwana wamkazi wa atate wako, kapena mwana wamkazi wa mai wako, wobadwa kwanu, kapena wobadwa kwina. 10Usamabvula mwana wamkazi wa mwana wamwamuna wako, kapena mwana wamkazi wa mwana wamkazi wako; pakuti thupi lao ndi lako. 11Usamabvula mwana wamkazi wa mkazi wa atate wako, amene anambala atate wako, ndiye mlongo wako. 12Usamabvula mlongo wa atate wako; ndiye wa cibale ca atate wako. 13Usamabvula mbale wa mai wako; popeza ndiye mbale wa mai wako. 14Usamabvula mbale wa atate wako; usamasendera kwa mkazi wace; ndiye mai wako. 15Usamabvula mpongozi wako; ndiye mkazi wa mwana wamwamuna wako; usamambvula. 16Usamabvula mkazi wa mbale wako; ndiye thupi la mbale wako. 17Usamabvula mkazi ndi mwana wamkazi wace; usamatenga mwana wamkazi wa mwana wamwamuna wace, kapena mwana wamkazi wa mwana wamkazi wace kumbvula; ndiwo abale; cocititsa manyazi ici. 18Usamtenga mkazi kumuonjezera kwa mbale wace, kumbvuta, kumbvula pamodzi ndi mnzace, akah ndi moyo mnzaceyo. 19Usamasendera kwa mkazi kumbvula pokhala ali padera cifukwa ca kudetsedwa kwace. 20Usagona naye mkazi wa mnansi wako, kudetsedwa naye limodzi. 21Ndipo usamapereka a mbumba yako kuwapitiriza kumoto cifukwa ca Moleke, usamaipsa dzina la Mulungu wako: Ine ndine Yehova. 22Usamagonana ndi mwamuna, monga amagonana ndi mkazi; conyansa ici. 23Ndipo usamagonana ndi nyama iri yonse, kudetsedwa nayo; kapena mkazi asamaima panyama, kugonana nayo; cisokonezo coopsa ici.

24Musamadzidetsa naco cimodzi ca izi; pakuti amitundu amene ndiwapitikitsa pamaso panu amadetsedwa nazo zonsezi; 25dziko lomwe lidetsedwa; cifukwa cace ndililanga, ndi dzikoli lisanza okhala m'mwemo. 26Koma inu, muzisunga malemba anga ndi maweruzo anga, osacita cimodzi conse ca zonyansa izi; ngakhale wa m'dziko ngakhale mlendo wakugonera pakati pa inu; 27(pakuti eni dziko okhalako, musanafike inu, anazicita zonyansa izi zonse, ndi dziko linadetsedwa) 28lingakusanzeni inunso dzikoli, polidetsa inu, monga linasanza mtundu wa anthu wokhalako musanafike inu. 29Pakuti ali yense akacita ciri conse ca zonyansa Izi, inde amene azicita idzasadzidwa pakati pa anthu a mtundu wao. 30Potero muzisunga cilangizo canga, ndi kusacita ziri zonse za miyambo yonyansayi anaicita musanafike inu, ndi kusadzidetsa nayo: Ine ndine Yehova Mulungu-wako.

Malamulo ena osiyanasiyana

1Ndipo Yehova ananena ndi Mose, ndi kuti, 2Nena ndi khamu lonse la ana a
Israyeli, nuti nao, Muzikhala oyera; pakuti ine ndine Yehova Mulungu wanu,
ndine woyera. 3Ali yense aopemai wace, ndi atate wace; nimusunge
masabata anga; Ine ndine Yehova Mulungu wanu. 4Musamatembenukira
mafano, kapena kudzipangira mulungu woyenga; Ine ndine Yehova Mulungu
wanu. 5Ndipo pamene muphera Yehova nsembe yoyamika, muiphere kuti
mulandiridwe. 6Tsiku lomwelo mwaipha, ndi m'mawa mwace muidye; ngati
katsalirako kanthu tsiku lacitatu, muzikatentha ndi moto. 7Akakadya konse
tsiku tacitatu kali conyansa, kosabvomerezeka: 8koma ali yense akudyako
adzasenza mphulupulu yace, popeza waipsa copatulidwa ca Yehova; ndi
munthuyo amsadze, kumcotsa kwa anthu a mtundu wace.
9Pakukolola dzinthu za m'dziko mwanu, usamakololetsa m'mphepete mwa
munda wako, nusamakunkha khunkha. 10Usamakunkha khunkha la m'munda
wako wamphesa, usamazitola zidagwazi za m'munda wako wamphesa;
uzisiyire wosauka ndi mlendo; Ine ndine Yehova Mulungu wanu. 11Musamaba,
kapena kunyenga, kapena kunamizana. 12Musamalumbira monama ndi
kuchula dzina langa, ungaipse dzina la Mulungu wako; Ine ndine
Yehova. 13Usamasautsa mnansi wako, kapena kulanda zace; mphotho yace ya
wolipidwa isakhale ndi iwe kufikira m'mawa. 14Usamatemberera wogontha;
usamaika cokhumudwitsa pamaso pa wosaona; koma uziopa Mulungu wako;
Ine ndine Yehova. 15Musamacita cisalungamo pakuwemza mlandu;
usamabvomereza munthu wosauka, kapena kulemekeza munthu womveka;
uweruze mlandu wa munthu mnzako molungama. 16Usamayendayenda
nusinjirira mwa anthu a mtundu wako; usamatsata mwazi wa mnansi wako;
Ine ndine Yehova. 17Usamamuda mbale wako mumtima mwako; umdzudzule
munthu mnzako ndithu, usadzitengera ucimo cifukwa ca
iye. 18Usamabwezera cilango, kapena kusunga kanthu kukhosi pa ana a anthu
a mtundu wako; koma uzikonda mnansi wako monga udzikonda wekha; Ine
ndine Yehova. 19Muzisunga malemba anga, Usamalola zoweta zako za
mitundu yosiyana zikwerane; usamabzala m'munda mwako mbeu za mitundu
iwiri; usamabvala cobvala ca nsaru za mitundu iwiri zosokonezana. 20Munthu
akagona ndi mkazi, ndiye mdzakazi, wopalidwa ubwenzi ndi mwamuna,
wosamuombola kapena wosapatsidwa ufulu, akwapulidwe; asawaphe, popeza
si mfulu mkaziyo. 21Ndipo adze nayo nsembe yace yoparamula kwa Yehova,
ku khomo la cihema cokomanako, ndiyo nkhosa yamphongo ikhale nsembe
yoparamula. 22Ndipo wansembe acite comtetezera ndi nkhosa yamphongo ya
nsembe yoparamula pamaso pa Yehova, cifukwa ca kucimwa adacimwaku;
ndipo adzakhululukidwa cifukwa ca kucimwa kwace adacimwaku. 23Ndipo
mukadzalowa m'dzikomo, ndi kubzalamitengo yamitundumitundu ikhale ya
cakudya, muziyese zipatso zao monga kusadulidwa kwao; zaka zitatu
muziyese zosadulidwa; zisadyedwa. 24Koma caka cacinai zipatso zace zonse
zikhale zopatulika, za kumlemekeza nazo Yehova. 25Caka cacisanu muzidya
zipatso zace, kuti zobala zace zikucurukireni inu; Ine ndine Yehova Mulungu
wanu. 26Musamadya kanthu ndi mwazi wace; musamacita nyanga, kapena
kuombeza ula. 27Musamameta mduliro, kapena kusenga m'mphepete mwa
ndebvu zanu, 28Musamadziceka matupi anu cifukwa ca akufa, kapena kutema
mpbini; Ine ndine Yehova. 29Usamaipsa mwana wako wamkazi ndi kumcititsa
cigololo; lingadzale ndi cigololo dzikoli, ndi kudzazidwa nazo zocititsa
manyazi. 30Muzisunga masabata anga, ndi kucitira ulemu malo anga
opatulika; Ine ndine Yehova. 31Musamatembenukira kwa obwebweta, kapena

anyanga; musawafuna, ndi kudetsedwa nao; Ine ndine Yehova Mulungu wanu. 32Pali aimvi uziwagwadira, nucitire ulemu munthu wokalamba; nuope Mulungu wako; lnendine Yehova. 33Ndipo mlendo akagonera m'dziko mwanu, musamamsautsa. 34Mlendo wakugonera kwa inu mumuyese pakati pa inu monga wa m'dziko momwemo; umkonde monga udzikonda wekha; popeza munali alendo m'dziko la Aigupto; Ine ndine Yehova Mulungu wanu. 35Musamacita cisalungamo poweruza mlandu, poyesa utali wace, kulemera kwace, kapena kucuruka kwace. 36Mukhale naco coyesera coona, miyeso yoona, era woona, bini woona; Ine ndine Yehova Mulungu wanu, amene ndinakuturutsani m'dziko la Aigupto. 37Ndipo musamalire malemba anga onse, ndi maweruzo anga onse, ndi kuwacita; Ine ndine Yehova.

Ziletsedwa cipembedzo ca Moleke ndi zoipa zina

1Ndipo Yehova ananena ndi Mose, ndi kuti, 2Unenenso kwa ana a Israyeli ndi
kuti, Ali yense wa ana a Israyeli, kapena wa alendo akukhala m'Israyeli,
amene apereka mbeu zace kwa Moleke, azimupha ndithu; anthu a m'dziko
amponye miyala. 3Ndipo nkhope yanga idzatsutsana naye munthuyo, ndi
kumsadza kumcotsa pakati pa anthu a mtundu wace; popeza anapereka a
mbeu zace kwa Moleke, kudetsa nako malo anga opatulika, ndi kuipsa dzina
langa lopatulika. 4Ndipo ngati anthu a m'dzikomo akambisa munthuyo
pang'ono ponse, pamene apereka a mbeu zace kwa Moleke, kuti
asamuphe; 5pamenepo nkhope yanga idzatsutsana naye munthuyo, ndi banja
lace, ndi kumsadza iye, ndi onse akumtsata ndi cigololo kukacita cigololo kwa
Moleke, kuwacotsa pakati pa anthu a mtundu wao. 6Ndipo munthu
wakutembenukira kwa obwebweta ndi anyanga kuwatsata ndi cigololo,
nkhope yanga idzatsutsana naye munthuyo, ndipo ndidzamsadza kumcotsa
pakati pa anthu a mtundu wace. 7Cifukwa cace dzipatuleni, nimukhale oyera;
pakuti Ine ndine Yehova Mulungu wanu. 8Ndipo musunge malemba anga ndi
kuwacita; Ine ndine Yehova wakupatula inu. 9Pakuti ali yense wakutemberera
atate wace kapena mai wace azimupha ndithu; watemberera atate wace
kapena mai wace; mwazi wace ukhale pamutu pace. 10Munthu akacita
cigololo ndi mkazi wa mwini, popeza wacita cigololo ndi mkazi wa mnansi
wace, awaphe nditho, mwamuna ndi mkazi onse awiri. 11Munthu akagona
naye mkazi wa atate wace, wabvula atate wace; awaphe ndithu onse awiri;
mwazi wao ukhale pamtu pao. 12Munthu akagona ndi mpongozi wace,
awaphe onse awiri; acita cisokonezo; mwazi wao ukhale pamtu pao. 13Munthu
akagonana ndi mwamuna mnzace, monga amagonana ndi mkazi, acita
conyansa onse awiri; awaphe ndithu; mwazi wao ukhale pamtu pao. 14Munthu
akatenga mkazi pamodzi ndi mai wace cocititsa manyazi ici; aziwatentha ndi
moto, iye ndi iwowa; kuti pasakhale cocititsa manyazico pakati pa
inu. 15Mwamuna akagona ndi nyama amuphe ndithu; muiphenso
nyamayi. 16Mkazi akasendera kwa nyama iri yonse kugonana nayo, umuphe
mkaziyo, ndi nyama yomwe; muwaphe ndithu; mwazi wao ukhale pamtu
pao. 17Munthu akatenga mlongo wace, mwana wamkazi wa atate wace,
kapena mwana wamkazi wa mai wace, nakaona thupi lace, ndi mlongoyo
akaona thupi lace; cocititsa manyazi ici; ndipo awasadze pamaso pa ana a
anthu ao; anabvula mlongo wace; asenze mphulupulu yace. 18Munthu
akagona ndi mkazi ali mumsambo, nakambvula, anabvula kasupe wace, ndi
iye mwini anabvula kasupe wa nthenda yace; awadule onse awiri pakati pa
anthu a mtundu wao. 19Usamabvula mbale wa mai wako, kapena mlongo wa
atate wako; popeza anabvula abale ace; asenze mphulupulu yao. 20Munthu
akagona ndi mkazi wa mbale wa atate wace, nabvula mbale wa atate wace;
asenze kucimwa kwao; adzafa osaona ana. 21Munthu akatenga mkazi wa
mbale wace, codetsa ici; wabvula mbale wace; adzakhala osaona ana.
22Potero muzisunga malemba anga onse, ndi maweruzo anga onse, kuwacita;
lingakusanzeni inu dziko limene ndipita nanuko, kuti mukhale
m'mwemo. 23Musamatsata miyambo ya mtundu umene neliucotsa pamaso
panu; popeza anacita izi zonse, nelinalema nao. 24Koma ndanena nanu,
Mudzalandira dziko lao inu, ndipo Ine ndilipereka kwa inu likhale lanu, ndilo
dziko moyenda mkaka ndi uci ngati madzi; Ine ndine Yehova Mulungu wanu
amene ndinakusiyanitsani ndi mitundu yina ya anthu. 25Potero musiyanitse
pakati pa nyama zoyera ndi nyama zodetsa, ndi pakati pa mbalame zodetsa
ndi zoyera; ndipo musadzinyansitsa ndi nyama, kapena mbalame, kapena ndi

kanthu kali konse kakukwawa pansi, kamene ndinakusiyanitsirani kakhale kodetsa. 26Ndipo muzikhala oyera kwa Ine; pakuti Ine Yehova ndine woyera, ndipo ndinakusiyanitsani kwa mitundu ya anthu mukhale anga. 27Munthu wamwamuna kapena wamkazi wakubwebweta, kapena wanyanga, azimupha ndithu; aziwaponya miyala; mwazi wao ukhale pamtu pao.

Za kupatulika kwa ansembe

1Ndipo Yehova ananena ndi Mose, Nena ndi ansembe, ana a Aroniwo, nuti nao, Asadzidetse mmodzi wa inu cifukwa ca wakufa mwa anthu a mtundu wace; 2koma cifukwa ca abale ace eni eni ndiwo, mai wace, ndi atate wace, ndi mwana wace wamwamuna, ndi mwana wace wamkazi, ndi mbale wace; 3ndi cifukwa ca mlongo wace weni weni, akakhala namwali wosakhala naye mwamuna, nkuloleka adzidetse cifukwa ca iwowa. 4Akakhala mwini banja pakati pa anthu a mtundu wace, asadzidetse, ndi kudziipsa, 5Asamete tsitsi la pamtu pao, kapena kucecerera ndebvu zao, kapena kudziceka matupi ao. 6Azikhala opatulikira Mulungu wao, osaipsa dzina la Mulungu wao; popeza amapereka nsembe zamoto za Yehova, mkate wa Mulungu wao; cifukwa cace akhale opatulika. 7Asadzitengere mkazi wacigololo, kapena woipsidwa; asatenge mkazi woti adamcotsa mwamuna wace; popeza apatulikira Mulungu wace. 8Cifukwa cace umpatule; popeza amapereka mkate wa Mulungu wako; umuyese wopatulika; pakuti Ine Yehova wakupatula iwe, ndine woyera, 9Akadziipsa mwana wamkazi wa wansembe ndi kucita cigololo, alikuipsa atate wace; amtenthe ndi moto.

10Ndipo iye wokhala mkulu wansembe mwa abale ace, amene anamtsanulira mafuta odzoza pamutu pace, amene anamdzaza dzanja kuti abvale zobvalazo, asawinde, kapena kung'amba zobvala zace. 11Asafike kuli mtembo; asadzidetse cifukwa ca atate wace, kapena mai wace. 12Asaturuke m'malo opatulika, kapena kuipsa malo opatulika a Mulungu wace; popeza korona wa mafuta odzoza wa Mulungu wace ali pa iye; Ine ndine Yehova. 13Ndipo adzitengere mkazi akali namwali. 14Mkazi wamasiye, kapena womleka, kapena woipsidwa, wacigololo, oterewa asawatenge; koma azitenga namwali wa anthu a mtundu wace akhale mkazi wace. 15Asaipse mbeu yace mwa anthu a mtundu wace; popeza Ine ndine Yehova wakumpatula iye.

Ansembe akhale opanda cirema pathupi

16Ndipo Yehova ananena ndi Mose, ndi kuti, 17Nena ndi Aroni, kuti, Ali yense wa mbeu zako mwa mibadwo yao wakukhala naco cirema, asayandikize kupereka mkate wa Mulungu wace. 18Pakuti munthu ali yense wokhala naco cirema, asayandikize; wakhungu, kapena wotsimphina, kapena wopunduka mph uno, kapena wamkuru ciwalo, 19kapena munthu wopunduka phazi kapena wopunduka dzanja, 20kapena wowerama, kapena wamfupi msinkhu, kapena wopunduka diso, kapena munthu wamphere, kapena wacipere, kapena wopunduka kumoto. 21Wa mbeu ya Aroni wansembe asayandikize mmodzi wokhala naco cirema, kupereka nsembe zamoto za Yehova; ali naco cirema asayandikize kupereka cakudya ca Mulungu wace. 22Adye cakudya ca Mulungu wace, copatulikitsa, ndi copatulika; 23koma asafike ku nsaru yocinga, asayandikize ku guwa la nsembe, popeza ali naco cirema; kuti angaipse malo anga opatulika; popeza Ine ndine Yehova wakuwapatula. 24Momwemo Mose ananena ndi Aroni, ndi ana ace amuna, ndi ana onse a Israyeli.

Ansembe ayere pakudya zopatulika

1Ndipo Yehova ananena ndi Mose, ndi kuti, 2Nena ndi Aroni ndi ana ace amuna, kuti azikhala padera ndi zinthu zopatulika za ana a Israyeli, zimene amandipatulira Ine, ndipo asaipse dzina langa loyera; Ine ndine Yehova. 3Nena nao, Ali yense wa mbeu zanu zonse mwa mibadwo yanu, akayandikiza zinthu zopatulika, zimene ana a Israyeli azipatulira Yehova, pokhala ali naco comdetsa cace, azimsadza munthuyo pankhope panga; Ine ndine Yehova. 4Munthu ali yense wa mbeu za Aroni wokhala ndi khate, kapena kukha, asadyeko zinthu zopatulika, kufikira atayera. Ndipo ali yense wokhudza cinthu codetsedwa ndi wakufa, kapena mwamuna wogona uipa; 5ndi ali yense wokhudza cinthu cokwawa cakudetsedwa naco, kapenanso munthu amene akamdetsa naco, codetsa cace ciri conse; 6munthu wokhudza ciri conse cotere adzakhala wodetsedwa kufikira madzulo, ndipo asadye zinthu zopatulika, akapanda kusamba thupi lace ndi madzi. 7Koma litalowa dzuwa, adzakhala woyera, ndi pambuyo pace adyeko zoyerazo, popeza ndizo cakudya cace. 8Asamadya zakufa zokha, kapena zojiwa, kudzidetsa nazo; Ine ndine Yehova. 9Potero asunge cilangizo canga, angasenzepo ucimo, ndi kufera m'mwemo, pakuciipsa; Ine ndine Yehova wakuwapatula iwo, 10Mlendo asadyeko copatulikaco; wakungokhala, ndi wansembe, kapena wolembedwa nchito, asadyeko copatulikaco. 11Koma wansembe atakagula munthu ndi ndarama zace, iyeyu adyeko; ndi iwo amene anabadwa m'nyumba yace, adyeko mkate wace. 12Ndipo mwana wamkazi wa wansembe akakwatibwa ndi mlendo, asadyeko nsembe yokweza ya zinthu zopatulika. 13Koma mwana wamkazi wa wansembe akakhala wamasiye kapena wocotsedwa, ndipo alibe mwana, nabwerera ku nyumba ya atate wace, monga muja anali mwana, adyeko mkate wa atate wace; koma mlendo asamadyako. 14Ndipo munthu akadyako cinthu copatulika mosadziwa, azionjezapo limodzi la magawo asanu, nalipereke kwa wansembe, pamodzi ndi copatulikaco. 15Potero asaipse zinthu zopatulika za ana a Israyeli, zopereka iwo kwa Yehova; 16ndi kuwasenzetsa mphulupulu yakuwaparamulitsa, pakudya iwo zopatulika zao; pakuti Ine ndine Yehova wakuwapatula.

Za nsembe zaufulu

17Ndipo Yehova ananena ndi Mose, ndi kuti, 18Nena ndi Aroni, ndi ana ace amuna, ndi ana onse a Israyeli, nuti nao, Ali yense wa mbumba ya Israyeli, kapena wa alendo ali m'Israyeli, akabwera naco copereka cace, monga mwa zowinda zao zonse, kapena monga mwa zopereka zaufulu zao, zimene abwera nazo kwa Yehova zikhale nsembe zopsereza; 19kuti mulandiridwe, azibwera navo yaimuna yopanda cirema, ya ng'ombe, kapena nkhosa, kapena mbuzi. 20Musamabwera nayo yokhala ndi cirema; popeza siidzalandirikira inu. 21Ndipo munthu akabwera nayo nsembe yoyamika kwa Yehova, ya pa cowinda cacikuru, kapena ya pa copereka caufulu, ya ng'ombe kapena nkhosa, ikhale yangwiro kuti ilandirike; ikhale yopanda cirema. 22Musamabwera nazo kwa Yehova yakhungu, kapenayodukamwendokapena yopunduka, kapena yapfundo, kapena yausemwe, kapena ya usemwe waukuru, musamazipereka kwa Yehova nsembe zamoto pa guwa la nsembe. 23Ng'ombe kapena nkhosa yokula kapena yocepa ciwalo, ikhale nsembe yaufulu; koma pa cowinda siidzalandirika. 24Nyama yofula, kapena copwanya kapena cosansantha, kapena cotudzula, kapena codula, musamabwera nazo kwa Yehova; inde musamacicita ici m'dziko mwanu. 25Ndipo musamazilandira izi ku dzanja la

mlendo ndi kubwera nazo zikhale cakudya ca Mulungu wanu; popeza ziri nako kubvunda kwao; ziri ndi cirema; sizidzalandirikira inu.
26Ndipo Yehova ananena ndi Mose, ndi kuti, Zikamabadwa ng'ombe kapena nkhosa, kapena mbuzi, zikhale ndi mace masiku asanu ndi awiri; 27kuyambira tsiku lacisanu ndi citatu ndi m'tsogolo mwace, idzalandirika ngati copereka nsembe yamoto ya Yehova. 28Koma musamaipha ng'ombe kapena nkhosa pamodzi ndi mwana wace tsiku limodzimodzi. 29Ndipo mukamaphera Yehova nsembe yoyamika, muiphere kuti mulandirike. 30Idyedwe tsiku lomwelo; musamasiyako kufikira m'mawa; Ine ndine Yehova. 31Potero muwasunge malamulo anga, ndi kuwacita; Ine ndine Yehova. 32Musamaipsa dzina langa loyera; koma ndikhale woyera pakati pa ana a Israyeli; Ine ndine Yehova wakukupatulani, 33amene ndinakuturutsani m'dziko la Aigupto, kuti ndikhale Mulungu wanu; Ine ndine Yehova.

Za nyengo zoikika za Yehova

1Ndipo Yehova ananena ndi Mose, ndi kuti, 2Nena ndi ana a Israyeli, nuti nao, Nyengo zoikika za Yehova zimene muzilalikira zikhale masonkhano opatulika, ndizo nyengo zanga zoikika. 3Masiku asanu ndi limodzi azigwira nchito; koma lacisanu ndi ciwiri ndilo Sabata lakupumula, msonkhano wopatulika; musamagwira nchito konse; ndilo sabata la Yehova m'nyumba zanu zonse.

Paskha

4Izi ndi nyengo zoikika za Yehova, masonkhano opatulika, zimene muzilalikira pa nyengo zoikika zao. 5Mwezi woyamba, tsiku lakhumi ndi cinai la mweziwo, madzulo, pali Paskha wa Yehova. 6Ndipo tsiku lakhumi ndi cisanu la mwezi womwewo ndilo madyerero a mkate wopanda cotupitsa a Yehova; masiku asanu ndi awiri muzidya mkate wopanda cotupitsa. 7Tsiku lace loyamba mukhale nao msonkhano wopatulika; musamagwira nchito ya masiku ena. 8Koma mubwere nayo kwa Yehova nsembe yamoto masiku asanu ndi awiri; pa tsiku lacisanu ndi ciwiri pakhale msonkhano wopatulika; musamacita nchito ya masiku ena.

Zipatso zoyamba

9Ndipo Yehova ananena ndi Mose, nati, 10Nena ndi ana a Israyeli, nuti nao, Mutakalowa m'dziko limene ndikupatsani, ndi kuceka dzinthu zace, pamenepo muzidza nao mtolo wa zipatso zoyamba za masika anu kwa wansembe; 11ndipo iye aweyule mtolowo pamaso pa Yehova, ulandirikire inu, tsiku lotsata sabata wansembe aweyule. 12Ndipo tsiku loweyula mtolowo, ukonze mwana wa nkhosa wopanda cirema, wa caka cimodzi, akhale nsembe yopsereza ya Yehova. 13Ndipo nsembe yaufa yace ikhale awiri a magawo khumi a ufa wosalala wosanganiza ndi mafuta, ndiyo nsembe yamoto ya Yehova, icite pfungo lokoma; ndi nsembe yace yothira ikhale yavinyo, limodzi la magawo anai la hini. 14Musamadya mkate, kapena tirigu wokazinga, kapena ngala zaziwisi, kufikira tsiku lomweli, kufikira mutadza naco copereka ca Mulungu wanu; ndilo lemba losatha mwa mibadwo yanu m'nyumba zanu zonse.

15Ndipo mudziwerengere kuyambira tsiku lotsata Sabata, kuyambira tsikuli mudadza nao mtolo wa nsembe yoweyula; pakhale masabata asanu ndi awiri amphumphu; 16muwerenge masiku makumi asanu kufikira tsiku lotsata sabata lacisanu ndi ciwiri; pamenepo mubwere nayo kwa Yehova nsembe ya ufa watsopano. 17Muturuke nayo m'zinyumba zanu mikate iwiri ya nsembe yoweyula, ikhale ya awiri a magawo khumi a efa; ikhale ya ufa wosalala, yopanga ndi cotupitsa, zipatso zoyamba za Yehova. 18Ndipo mubwere nao pamodzi ndi mikate, ana a nkhosa asanu ndi awiri, opanda cirema a caka cimodzi, ndi ng'ombe yamphongo imodzi, ndi nkhosa zamphongo ziwiri; zikhale nsembe yopsereza ya Yehova, pamodzi ndi nsembe yao yaufa, ndi nsembe zao zothira, ndizo nsembe yamoto ya pfungo lokoma la Yehova. 19Mukonzenso mwana wa mbuzi mmodzi akhale nsembe yaucimo, ndi ana a nkhosa awiri a caka cimodzi akhale nsembe yoyamika. 20Ndi wansembe awaweyule, pamodzi ndi mkate wa zipatso zoyamba, nsembe yoweyula pamaso pa Yehova, pamodzi ndi ana a nkhosa awiriwo; zikhale zopatulikira Yehova, kuti zikhale za wansembe. 21Ndipo mulalikire tsiku lomwelo; kuti mukhale nao msonkhano wopatulika; musamagwira nchito ya masiku ena; ndilo lemba losatha m'nyumba zanu zonse, mwa mibadwo yanu yonse.

22Ndipo pakukolola dzinthu za m'dziko mwanu, usamakololetsa m'mphepete
mwa munda wako, nusamakunkha khunkha; uzisiyire wosauka ndi mlendo;
Ine ndine Yehova Mulungu wako.
23Ndipo Yehova ananena ndi Mose, ndi kuti, 24Nena ndi ana a Israyeli, ndi
kuti, Mwezi wacisanu ndi ciwiri, tsiku loyamba la mweziwo, muzipumula, ndiko
cikumbutso ca kuliza malipenga, msonkhano wopatulika. 25Musamagwira
nchito ya masiku ena; mubwere nayo nsembe yamoto ya Yehova.

Tsiku la citetezero

26Ndipo Yehova ananena ndi Mose, ndi kuti, 27Komatu, tsiku lakhumi la mwezi
uwu wacisanu ndi ciwiri, ndilo tsiku la citetezero; mukhale nao msonkhano
wopatulika, ndipo mudzicepetse; ndi kubwera nayo nsembe yamoto kwa
Yehova. 28Musamagwira nchito iri yonse tsiku limenelo; pakuti ndilo tsiku la
citetezero, kucita cotetezera inu pamaso pa Yehova Mulungu wanu. 29Pakuti
munthu ali yense wosadzicepetsa tsiku limenelo, amsadze kwa anthu a
mtundu wace. 30Ndi munthu ali yense wakugwira nchito iri yonse tsiku
limenelo, ndidzaononga munthuyo pakati pa anthu a mtundu
wace. 31Musamagwira nchito iri yonse; ndilo lemba losatha mwa mibadwo
yanu, m'nyumba zanu zoo nse. 32Likhale ndi inu Sabata lakupumula; ndipo
mudzicepetse; tsiku lacisanu ndi cinai madzulo, kuyambira madzulo kufikira
madzulo musunge Sabata lanu.

Madyerero a misasa

33Ndipo Yehova ananena ndi Mose, ndi kuti, 34Nena ndi ana a Israyeli, kuti,
Tsiku lakhumi ndi cisanu la mwezi uno wacisanu ndi ciwiri pali madyerero a
misasa a Yehova, masiku asanu ndi awiri. 35Tsiku loyamba likhale msonkhano
wopatulika, musamagwira nchito ya masiku ena. 36Masiku asanu ndi awiri
mubwere nayo nsembe yamoto kwa Yehova; tsiku lacisanu ndi citatu mukhale
nao msonkhano wopatulika; ndipo mubwere nayo nsembe yamoto kwa
Yehova; ndilo lotsirizira; musamagwira nchito ya masiku ena.
37Izi ndi nyengo zoikika za Yehova, zimene muzilalikira zikhale masonkhano
opatulika, kukabwera nayo nsembe yamoto kwa Yehova, nsembe yopsereza,
ndi nsembe yaufa, nsembe yophera, ndi nsembe yothira, yonse pa tsiku lace
lace; 38pamodzi ndi masabata a Yehova, ndi pamodzi ndi mphatso zanu, ndi
pamodzi ndi zoo winda zanu zonse, ndi pamodzi ndi zopereka zaufulu zanu,
zimene muzipereka kwa Yehova.
39Koma tsiku lakhumi ndi cisanu la mwezi wacisanu ndi ciwiri, mutatuta
zipatso za m'dziko, muzisunga madyerero a Yehova masiku asanu ndi awiri;
tsiku loyamba mupumule, ndi tsiku lacisanu ndi citatu mupumule. 40Ndipo
tsiku loyambali mudzitengere nthambi za mitengo yokoma, nsomo za
kanjedza, ndi nthambi za mitengo yobvalira, ndi misondodzi ya kumtsinje;
ndipo mukondwere pamaso pa Yehova Mulungu wanu masiku asanu ndi
awiri. 41Ndipo muwasunge madyerero a Yehova masiku asanu ndi awiri
m'caka; ndilo lemba losatha mwa mibadwo yanu; musunge mwezi wacisanu
ndi ciwiri. 42Mukhale m'misasa masiku asanu ndi awiri; onse obadwa m'dziko
mwa Israyeli akhale m'misasa; 43kuti mibadwo yanu ikadziwe lruti
ndinakhalitsa ana a Israyeli m'misasa, pamene ndinawaturutsa m'dziko la
Aigupto; Ine ndine Yehova Mulungu wanu. 44Ndipo Mose anafotokozera ana a
Israyeli nyengo zoikika za Yehova.

Za mafuta a nyalizo ndi mkate woonekera

1Ndipo Yehova ananena ndi Mose, ndi kuti, 2Uza ana a Israyeli, kuti akutengere mafuta a azitona oyera opera akuunikira, kuti aziwalitsa nyali nthawi zonse. 3Aroni aikonze kunja kwa nsaru yocinga ya mboni, m'cihema cokomanako, kuyambira madzulo kufikira m'mawa, pamaso pa Yehova nthawi zonse; likhale lemba losatha mwa mibadwo yanu. 4Akonze nyalizo pa coikapo nyali coona pamaso pa Yehova nthawi zonse.

5Ndipo uzitenga ufa wosalala, ndi kuphika timitanda khumi ndi tiwiri; awiri a magawo khumi a efa afikane kamtanda kamodzi, 6Ndipo utiike m'mizere iwiri, tisanu ndi kamodzi mzere umodzi, pa gome loyera, pamaso pa Yehova. 7Nuike libano loona ku mzere uli wonse, kuti likhale kumkate ngati cokumbutsa, nsembe yamoto ya Yehova. 8Nthawi zonse tsiku la Sabata aukonze pamaso pa Yehova, cifukwa ca ana a Israyeli, ndilo pangano losatha. 9Ndipo ukhale wa Aroni ndi ana ace, audye pamalo popatulika; pakuti auyese wopatulikitsa wocokera ku nsembe zamoto za Yehova; ndilo lemba losatha.

Kulangidwa kwa wotemberera Mulungu ndi ocimwira zina

10Ndipo mwana wamwamuna wa mkazi M-israyeli, atate wace ndiye M-aigupto, anaturuka mwa ana a Israyeli; ndi mwana wamwamuna wa mkazi M-israyeliyo analimbana naye munthu M-israyeli kucigono; 11ndipo mwana wamwamuna wa mkazi M-israyeli anacitira DZINA mwano, natemberera; ndipo anadza naye kwa Mose. Dzina la mai wace ndiye Selomiti, mwana wa Dibri, wa pfuko la Dani. 12Ndipo anamsunga m'kaidi, kuti awafotokozere m'mene anenere Yehova.

13Ndipo Yehova ananena ndi Mose, nati, 14Turuka naye wotembererayo kunja kwa cigono; ndipo onse adamumva aike manja ao pamutu pace, ndi khamu lonse limponye miyala afe. 15Ndipo unene ndi ana a Israyeli, ndi kuti, Ali yense wotemberera Mulungu wace azisenza kucimwa kwace. 16Ndi iye wakucitira mwano dzina la Yehova, amuphe ndithu; khamu lonse limponye miyala ndithu; mlendo ndi wobadwa m'dziko yemwe akacitira dzina la Yehova mwano, awaphe. 17Munthu akakantha munthu mnzace ali yense kuti afe, amuphe ndithu. 18Munthu akakantha nyama kuti ife, ambwezere yina; moyo kulipa moyo. 19Munthu akacititsa mnansi wace cirema, monga umo anacitira momwemo amcitire iye; 20kutyola kulipa kutyola, diso kulipa diso, dzino kulipa dzino; monga umo anacitira munthu cirema, momwemo amcitire iye. 21Iye wakukantha nyama kuti ife, ambwezere yina; iye wakupha munthu, amuphe. 22Ciweruzo canu cifanefane ndi mlendo ndi wobadwa m'dziko; pakuti Ine ndine Yehova Mulungu wanu. 23Ndipo Mose ananena ndi ana a Israyeli, ndipo anaturutsa wotembererayo kunja kwa cigono, namponya miyala. Ndipo ana a Israyeli anacita monga Yehova adauza Mose.

Za caka copumula dziko

1Ndipo Yehova ananena ndi Mose m'phiri la Sinai, ndi kuti, 2Nena ndi ana a
Israyeli, nuti nao, Mutakalowa m'dziko limene ndikupatsani, dzikoli lizisungira
Yehova Sabata. 3Zaka zisanu ndi cimodzi ubzale m'munda mwako, ndi zaka
zisanu ndi cimodzi udzombole mphesa zako, ndi kuceka zipatso zace; 4koma
caka cacisanu ndi ciwiri cikhale sabata lakupumula la dziko, sabata la Yehova;
usamabzala m'munda mwako, usamadzombola mipesa yako. 5Zophuka zokha
zofikira masika usamazichera, ndi mphesa za mipesa yako yosadzombola
usaziceka; cikhale caka copumula dziko. 6Ndipo sabata la dzikoli likhale kwa
inu la cakudya; kwa iwe, ndi mnyamata wako, ndi mdzakazi wako, ndi
wolembedwa nchito yako, ndi mlendo wako wakugonera kwanu; 7ndi ng'ombe
zako, ndi nyama ziri m'dziko lako; zipatso zace zonse zikhale cakudya cao.

Za caka coliza lipenga

8Ndipo uziwerengera masabata a zaka asanu ndi awiri, zaka zisanu ndi ziwiri
kasanu ndi kawiri; kotero kuti zaka za masabata a zaka asanu ndi awiri, zifikire
zaka makumi anai kudza zisanu ndi zinai. 9Pamenepo uzitumizira lipenga
lomveka m'mwezi wacisanu ndi ciwiri, tsiku lakhumi la mweziwo; tsiku la
citetezero mutumizire lipenga lifikire m'dziko lanu lonse. 10Ndipo mucipatule
caka ca makumi asanu, ndi kulalikira kwa onse okhala m'dzikomo kuti akhale
aufulu; muciyese caka coliza lipenga; ndipo mubwerere munthu ali yense ku
zace zace, ndipo mubwerere yense ku banja lace. 11Muciyese caka ca makomi
asanuco coliza lipenga, musamabzala, kapena kuceka zophuka zokha
m'mwemo; kapenakuceka mphesa zace za mipesa yosadzombola. 12Popeza
ndico caka coliza lipenga; muciyese copatulika, mudye zipatso zace kunja kwa
munda. 13Caka coliza lipenga ici mubwerere nonse ku zace zace. 14Ndipo
ukagulitsa kanthu kwa mnansi wako, kapena kugula kanthu ka mnansi wako,
musamasautsana; 15monga mwa kuwerenga kwace kwa zaka, citapita coliza
lipenga, uzigula kwa mnansi wako, ndi monga mwa kuwerenga kwa zaka za
zipatso azigulitsa. 16Monga mwa kucuruka kwa zaka zace uonjeze mtengo
wace, ndi monga mwa kucepa kwa zaka zace ucepse mtengo wace; pakuti
akugulitsa powerenga masiku ace. 17Musamasautsana, koma uope Mulungu
wako; popeza Ine ndine Yehova Mulungu wanu. 18M'mwemo mucite malemba
anga, ndi kusunga maweruzo anga, ndi kuwacita; ndipo mudzakhala
m'dzikomo okhazikika. 19Dziko lidzaperekanso zipatso zace, ndipo mudzadya
ndi kukhuta, ndi k'ukhalamo okhazikika. 20Ndipo mukadzati, Tidzadyanji caka
cacisanu ndi ciwiri? taonani, sitidzabzala, sitidzakolola dzinthu; 21pamenepo
ndidzauza dalitso langa litsike pa inu caka cacisanu ndi cimodzi, ndipo
cidzapatsa zipatso zofikira zaka zitatu. 22Ndipo mubzale caka cacisanu ndi
citatu, ndi kudya zipatso zasundwe; kufikira caka cacisanu ndi cinai, mpaka
zitacha zipatso zace mudzadya zasundwe.

Za kuombola dziko ndi nyumba

23Ndipo asaligulitse dziko cigulitsire; popeza dzikoli ndi langa; pakuti inu ndinu
alendo akugonera ndi Ine. 24Potero muzilola liomboledwe dziko lonse muli
nalo.

25Mbale wako akasaukira cuma, nakagulitsa cace cace, pamenepo mombolo
wace, mbale wace weni weni azidza, naombole cimene mbale wace
anagulitsaco. 26Ndipo munthu akasowa mombolo, koma dzanja lace
lacionetsa, nacipeza cofikira kuciombola; 27pamenepo awerenge zaka za
kugulitsa kwace, nabwezere wosulayo zotsalirapo, nabwerere iye ku dziko
lace. 28Koma dzanja lace likapanda kupeza zofikira za kumbwezera,

pamenepo cogulitsaco cikhale m'dzanja lace la iye adacigulayo, kufikira caka coliza lipenga; koma caka coliza lipenga cituruke, nabwerere iye ku dziko lace.
29Munthu akagulitsa nyumba yogonamo, m'mudzi wa m'linga, aiombole cisanathe caka coigulitsa; kufikira kutha caka akhoza kuombola. 30Ndipo akapanda kuiombola kufikira kutha kwace kwa caka camphumphu, nyumba iri m'mudzi wa m'lingayi idzakhala yace ya iye adaigula yosamcokeranso mwa mibadwo yace; siidzaturuka caka coliza lipenga. 31Koma nyumba za m'midzi yopanda linga aziyese monga minda ya m'dziko; ziomboledwe, zituruke m'caka coliza lipenga. 32Kunena za midzi ya Alevi, nyumba za m'midzi yao yao, Alevi akhoza kuziombola nthawi zonse. 33Ndipo munthu akagula kwa Mlevi, nyumba yogulayo yokhala m'mudzi wace wace, ituruke m'caka coliza lipenga, popeza nyumba za m'midzi ya Alevi ndizo zao zao mwa ana a Israyeli. 34Koma dambo la podyera pao siligulika; popeza ndilo lao lao kosatha.
35Ndipo mbale wako akasaukira cuma, ndi dzanja lace lisowa; iwe uzimgwiriziza; akhale nawe monga mlendo wakugonera kwanu. 36Usamambwezetsa phindu, kapena cioniezero; koma uope Mulungu wako; kuti mbale wako akhale nawe. 37Musamampatsa ndarama zako polira phindu, kapena kumpatsa zakudya kuti aonjezerepo pocibwezera. 38Ine ndine Yehova Mulungu wanu, amene ndinakuturutsani m'dziko la Aigupto, kukupatsani dziko la Kanani, kuti ndikhale Mulungu wanu.

Za mbale wodzigulitsa akhale kapolo

39Ndipo mbale wako akasaukira cuma, ndi kudzigulitsa kwa iwe; usamamgwiritsa nchito monga kapolo; 40azikhala nawe ngati wolipidwa nchito, ngati munthu wokhala nawe; akutumikire kufikira caka coliza lipenga. 41Pamenepo azituruka kukucokera, iye ndi ana ace omwe, nabwerere ku mbumba yace; abwerere ku dziko lao lao la makolo ace. 42Pakuti iwo ndiwo atumiki anga, amene ndinawaturutsa m'dziko la Aigupto; asamawagulitsa monga amagulitsa kapolo. 43Usamamweruza momzunza; koma uope Mulungu wako. 44Kunena za kapolo wako wamwamuna, kapena wamkazi amene ukhala nao; azikhala a amitundu akuzungulira inu, kwa iwowa muzigula akapolo amuna ndi akazi. 45Muwagulenso ana a alendo akukhala mwa inu, a iwowa ndi a mabanja ao akukhala nanu, amene anabadwa m'dziko lanu; ndipo adzakhala anu anu. 46Ndipo muwayese colowa ca ana anu akudza m'mbuyo, akhale ao ao; muwayese akapolo kosatha; koma za abale anu, ana a Israyeli, musamalamulirana mozunza.
47Ndipo mlendo wakugonera kwanu akalemera cuma, ndi mbale wako wakukhala naye akasauka, nadzigulitsa kwa mlendo wakugonera kwanu, kapena kwa pfuko la banja la mlendo; 48atatha kudzigulitsa, aomboledwe; wina wa abale ace amuombole; 49kapena mbale wa atate wace, kapena mwana wa mbale wa atate wace amuombole, kapena mbale wace ali yense wa banja lace amuombole; kapena akalemera cuma yekha adziombole yekha. 50Ndipo awerengere amene anamgulayo kuyambira caka adadzigulitsa kwa iye kufikira caka coliza lipenga; ndipo mtengo wace ukhale monga mwa kuwerenga kwa zaka; amuyesere monga masiku a munthu wolipidwa. 51Zikamtsalira zaka zambiri, monga mwa izi abwezere ndarama zakumuombola zocokera ku ndalama zomgulazo. 52Ndipo zikamtsalira zaka pang'ono kufikira caka coliza lipenga amwerengere; monga mwa zaka zace abwezere mtengo wace wakumuombola. 53Akhale naye monga wolipidwa caka ndi caka; asamamlamulira momzunza pamaso pako, 54Ndipo akapanda kumuombola motero, azituruka caka coliza lipenga, iye ndi ana ace

omwe. 55Pakuti ana a Israyeli ndi atumiki anga; iwo ndiwo atumiki anga amene ndinawaturutsa m'dziko la Aigupto; Ine ndine Yehova Mulungu wanu.

Malamulo, malonjezo, ndi macenjezo

1Musamadzipangira mafano, kapena kudziutsira mafano osema, kapena
coimiritsa, kapena kuika mwala wozokota m'dziko mwanu kuugwadira umene;
popeza Ine ndine Yehova Mulungu wanu. 2Musunge masabata anga, ndi
kucitira ulemu malo anga opatulika; Ine ndine Yehova.
3Mukamayenda m'malemba anga, ndi kusunga malamulo anga, ndi
kuwacita; 4ndidzakupatsani mvula m'nyengo zace, ndi dziko lidzapereka
zipatso zace, ndi mitengo ya m'minda idzabala zipatso zace. 5Ndipo nyengo
yopuntha tirigu idzafikira nyengo yochera mphesa, ndi nyengo yochera
mphesa idzafikira nyengo zobzala; ndipo mudzakhuta naco cakudya canu, ndi
kukhala m'dziko mwanu okhazikika. 6Ndipo ndidzapatsa mtendere m'dzikomo,
kuti mudzagone pansi, wopanda wina wakukuopsani; ndidzaletsanso zirombo
zisakhale m'dzikomo, lupanga lomwe silidzapita m'dziko
mwanu. 7Mudzapitikitsa adani anu, ndipo adzagwa pamaso panu ndi
lupanga, 8Asanu ainu adzapitikitsa zana limodzi, ndi zana limodzi la inu
adzapitikitsa zikwi khumi; ndi adani anu adzagwa pamaso panu ndi
lupanga. 9Ndipo ndidzatembenukira kwa inu, ndi kukubalitsani, ndi
kukucurukitsani; ndipo ndidzakhazika cipangano canga ndinapangana
nanuco. 10Ndipo mudzadya za sundwe wakale ndi kuturutsa zakale cifukwa ca
zatsopano. 11Ndidzamanga kacisi wanga pakati pa inu, ndipo moyo wanga
sudzanyansidwa nanu. 12Ndipo ndidzayendayenda pakati pa inu, ndi kukhala
Mulungu wanu ndi inu mudzakhala anthu anga. 13Ine ndine Yehova Mulungu
wanu, amene ndinakuturutsani m'dziko la Aigupto, kuti musakhale akapolo ao;
ndipo ndinatyola mitengo ya magoli anu, ndi kukuyendetsani coweramuka.
14Koma mukapanda kundimvera Ine, osacita malamulo awa onse; 15ndipo
mukakaniza malemba anga, ndi moyo wanu ukanyansidwa nao maweruzo
anga, kotero kuti simudzacita malamulo anga onse, koma kutyola cipangano
canga; 16ndidzacitira inu icinso; ndidzakuikirani zoopsa,
nthendayoondetsayam'cifuwa ndi malungo, zakulanda maso ndi mphamvu,
ndi kuzunza moyo; ndipo mudzabzala mbeu zanu cabe, pope za adani anu
adzazidya. 17Ndipt nkhope yanga idzatsutsana nanu kuti adani anu
adzakukanthani, ndipt akudana ndi inu adzacita ufumu Pl inu ndipo
mudzathawa wopanda wakukulondolani. 18Ndipo muka panda kundimvera,
zingakhale izi ndidzaonjeza kukulangani kasanu nd kawiri cifukwa ca zocimwa
zanu. 19Popeza ndidzatyola mphamvu yam yodzikuza; ndi kusandutsa thambo
lanu likhale ngati citsulo ndi dziko lanu ngati mkuwa; 20ndipo mudzacita nayo
mphamvu yanu cabe; ndi nthaka yanu siidzapereka zipatse zace, ndi mitengo
ya m'dziko siidzabala zobala zace. 21Ndipo mukayenda motsutsana nane,
osalola kumvera Ine; ndidzakuonjezerani miliri kasanu ndi kawiri, monga mwa
zocimwa zanu. 22Popeza ndidzatumiza cirombo ca kuthengo pakati pa inu,
ndipo cidzalanda ana anu, ndi kuononga zoweta zanu nicidzacepetsa inu kuti
mukhale pang'ono; ndi njira zanu zidzakhala zakufa. 23Ndipo mukapanda
kulangika nazo ndi kubwera kwa Ine, mukayenda motsutsana ndi
Ine; 24Inenso ndidzayenda motsutsana ndi inu; ndipo ndidzakukanthani Inedi
kasanu ndi kawiri cifukwa ca zoipa zanu. 25Ndipo ndidzadzetsa kwa inu
lupanga lakucita cilango ca cipangano; kotero kuti mudzasonkhanidwa
m'midzi mwanu; ndipo ndidzatumiza mliri pakati pa inu; ndipo
mudzaperekedwa m'manja mwa mdani. 26Pamene ndityola mcirikizo wanu wa
mkate, akazi khumi adzaphika mkate wanu mu mcembo umodzi, nadzabweza
mkate wanu ndi kuuyesa; ndipo mudzadya, koma osakhuta.

27Ndipo mukapanda kundimvera Ine, cingakhale ici, ndi kuyenda motsutsana
nane; 28Ine ndidzayenda nanu motsutsana mwa kukuzazirani, ndi kukulangani
Inedi kasanu ndi kawiri cifukwa ca zocimwa zanu. 29Ndipo mudzadya nyama
ya ana anu amuna; inde nyama ya ana anu akazi mudzaidya. 30Ndipo
ndidzaononga malo amsanje anu, ndi kulikha zoimiritsa zanu za dzuwa, ndi
kuponya mitembo yanu pa mitembo ya mafano anu; ndi moyo wanga
udzanyansidwa nanu. 31Ndipo ndidzasandutsa midzi yanu bwinja, ndi
kupasula malo anu opatulika, wosanunkhiza Ine za pfungo lanu
lokoma. 32Inde, ndidzapasula dzikoli, ndipo adani anu akukhala m'mwemo
adzadabwa nako. 33Ndipo ndidzabalalitsa inu mwa amitundu, ndi kusolola
lupanga kukutsatani; ndi dziko lanu lidzakhala lopasuka, ndi midzi yanu
idzakhala bwinja. 34Pamenepo dzikoli lidzakondwera nao masabata ace,
masiku onse a kupasuka kwace, pokhala inu m'dziko la adani anu; pamenepo
dziko lidzapumula, ndi kukondwera nao masabata ace. 35Masiku onse a
kupasuka kwace lipumula; ndiko mpumulo udalisowa m'masabata anu,
pokhala inu pamenepo. 36Kunena za iwo akutsalira, ndidzalonga kukomoka
kumtima kwao m'maiko a adani ao; ndi liu la tsamba lotengeka ndi mphepo
lidzawapitikitsa; ndipo adzathawa monga amathawa lupanga; ndipo adzagwa
wopanda wakuwalondola. 37Ndipo adzakhumudwitsana monga pothawa
lupanga, wopanda wakuwalondola; ndipo mudzakhala opanda mphamvu
yakuima pamaso pa adani anu. 38Ndipo mudzatayika mwa amitundu, ndi
dziko la adani anu lidzakudyani. 39Ndipo otsala mwa inu adzazunzika m'moyo
ndi mphulupulu zao m'maiko a adani anu; ndiponso ndi mphulupulu za makolo
ao adzazunzika m'moyo. 40Pamenepo adzabvomereza mphulupulu zao, ndi
mphulupulu za makolo ao, pocita zosakhulupirika pa Ine; ndiponso popeza
anayenda motsutsana ndi Ine, 41Inenso ndinayenda motsutsana nao, ndi
kuwatengera ku dziko la adani ao. Ngati tsono mtima wao wosadulidwa
udzicepetsa, ndipo abvomereza kulanga kwa mphulupulu zao; 42pamenepo
ndidzakumbukila pangano langa ndi Yakobo; ndiponso pangano langa ndi
Isake, ndiponso pangano langa ndi Abrahamu ndidzakumbukila; ndipo
ndidzakumbukila dzikoli. 43Dziko lomwe lidzasiyidwa nao, ndi kukondwera ndi
masabata ace, pokhala lopasuka, iwowa palibe; ndipo iwo adzabvomereza
kulanga kwa mphulupulu zao; popeza, inde popeza anakaniza maweruzo
anga, ndi moyo wao unanyansidwa nao malemba anga. 44Ndiponso pali
icinso: pokhala iwo m'dziko la adani ao sindidzawakaniza, kapena
kunyansidwa nao, kuwaononga konse, ndi kutyola pangano langa
ndinapangana nao; popeza Ine ndine Yehova Muhmgu wao. 45Koma cifukwa
ca iwo ndidzawakumbukila pangano la makolo ao, amene ndinawaturutsa
m'dziko la Aigupto pamaso pa amitundu, kuti ndikhale Mulungu wao; Ine
ndine Yehova. 46Awa ndi malemba ndi maweruzo ndi malamulo amene
Yehova anaika pakati pa iye ndi ana a Israyeli m'phiri la Sinai, ndi dzanja la
Mose.

Cowinda ndi ciombolo cace

1Ndipo Yehova ananena ndi Mose, ndi kuti, 2Nena ndi ana a Israyeli, nuti nao, Pamene munthu acita cowinda ca padera, anthuwo azikhala a Yehova monga mwa kuyesa kwako. 3Ukayesa wamwamuna wa zaka makumi awiri kufikira wina wa zaka makumi asanu ndi limodzi, uziwayesera a masekeli makumi asanu a siliva, monga mwa sekeli wa malo opatulika. 4Koma akakhala wamkazi, umuyesere wa masekeli makumi atatu. 5Akakhala munthu wa zaka zisanu kufikira wina wa zaka makumi awiri uwayesere, wamwamuna wa masekeli makumi awiri, ndi wamkazi wa masekeli khumi. 6Akakhala mwana wa mwezi umodzi kufikira zaka zisanu, uziwayesera wamwamuna wa masekeli asanu a siliva, ndi wamkazi wa masekeli atatu a siliva. 7Akakhala munthu wa zaka makumi asanu ndi limodzi ndi mphambu, akakhala wamwamuna, umuyesere wa masekeli khumi ndi asanu, akakhala wamkazi wa masekeli khumi. 8Koma cuma cace cikapanda kufikira kuyesa kwako, amuike pamaso pa wansembe, kuti wansembeyo amuyese; ndipo wansembeyo amuyese, monga akhoza iye amene anawinda.

9Ndipo cikakhala ca nyama imene anthu amabwera nayo ikhale copereka ca Yehova, zonse zotere munthu akazipereka kwa Yehova zikhale zopatulika. 10Asaisinthe, yokoma m'malo mwa yoipa, kapena yoipa m'malo mwa yokoma; ndipo akasinthadi nyama m'malo mwa inzace, pamenepo iyo ndi yosinthikayo zikhale zopatulika. 11Ndipo cikakhala ca nyama yodetsa, imene sabwera nayo ikhale copereka ca Yehova, aike nyamayi pamaso pa wansembe; 12ndipo wansembeyo aiyese mtengo wace, ingakhale yokoma kapena yoipa; monga uiyesa wansembewe, momwemo. 13Ndipo akaiombola ndithu, pamenepo aonjezepo limodzi la magawo asanu la mtengo wace.

14Munthu akapatula nyumba yace ikhale yopatulika kwa Yehova, wansembe aziiyesa mtengo wace, ingakhale yokoma kapena yoipa; monga wansembeyo aiyesa, ikhale momwemo. 15Ndipo iye wakuipatula akaombola nyumba yace, aonjezepo limodzi la magawo asanu la ndalama za kuyesa kwako, ndipo idzakhala yace.

16Munthu akapatulirako Yehova munda wace wace, uziuyesa monga mwa mbeu zace zikakhala; homeri wa barie uuyese wa masekeli makumi asanu a siliva. 17Akapatula munda wace kuyambira caka coliza lipenga, mundawo ukhale monga momwe unauyesera. 18Akaupatula munda wace citapita caka coliza lipenga, wansembe azimwerengera ndalama monga mwa zaka zotsalira kufikira caka coliza lipenga, nazicepsako pa kuyesa kwako. 19Ndipo wakupacula mundayo akauomboladi, aonjezeko limodzi la magawo asanu la ndalama za kuyesa kwako, ndipo uzikhalitsa wace. 20Koma akapanda kuombola mundawo, kapena atagulitsa mundawo kwa munthu wina, suomboledwanso; 21koma poturuka m'caka coliza lipenga, mundawo ukhale wopatulikira Yehova, ngati munda woperekedwa ciperekere kwa Mulungu; ukhale wace wace wa wansembe. 22Ndipo akapatulira Yehova munda woti adaugula, wosati wogawako ku munda wace wace; 23pamenepo wansembeyo amwerengere mtengo wace wa kuyesa kwako kufikira caka coliza lipenga; ndipo apereke kuyesa kwako tsiku lomwelo, cikhale cinthu copatulikira Yehova, 24Caka coliza lipenga mundawo ubwerere kwa iye amene adaugulitsa, kwa iye amene dzikoli ndi lace lace. 25Ndipo kuyesa kwako konse kukhale monga mwa sekeli wa malo opatulika; sekeli ndi magera makumi awiri.

26Komatu woyamba kubadwa mwa nyama akhale wobadwa woyamba wa Yehova, munthu asampatule; ingakhale ng'ombe ingakhale nkhosa, ndiye wa

Yehova. 27Koma akakhala wa nyama zodetsa, azimuombola monga mwa
kuyesa kwako, naonjezepo limodzi la magawo asanu la mtengo wace; ndipo
akapanda kumuombola, amgulitse monga mwa kuyesa kwako.

Za coperekedwa ciperekere, ndi Lakhumi La za nthaka ndi za m'khola

28Koma asacigulitse kapena kuciombola cinthu coperekedwa ciperekere kwa
Mulungu, cimene munthu acipereka ciperekere kwa: Yehova, cotengako ku
zonse ali nazo, ngakhale munthu, kapena nyama, kapena munda wace wace;
ciri conse coperekedwa ciperekere kwa Mulungu
neopatulikitsa. 29Asamuombole munthu woperekedwa ciperekere kwa
Mulungu; amuphe ndithu.
30Limodzi mwa magawo khumi la zonse m'dziko, la mbeu zace za dziko, la
zipatso za mtengo, ndilo la Yehova; likhale lopatulikira Yehova. 31Koma
munthu akaombolatu kanthu ka limodzi la magawo khumiwo aonjezeko
limodzi la magawo asanu. 32Ndipo limodzi la magawo khumi lonse la
ng'ombe, kapena la nkhosa, kapena la mbuzi, ziri zonse zimapita pansi pa
ndodo, limodzi la magawo khumi likhale lopatulikira Yehova. 33Asafunse ngati
yabwino kapena yoipa, kapena kuisintha; koma akaisinthatu, pamenepo iyo
ndi yosinthikayo zikhale zopatulika zonse ziwiri; asamaiombola.
34Awa ndi malamulo, amene Yehova anauza Mose, awauze ana a Israyeli,
m'phiri la Sinai.

Numbers

Numeri 1

Aisrayeli awerengedwa m'cipululu ca Sinai

1NDIPO Yehova ananena ndi Mose m'cipululu ca Sinai, m'cihema cokomanako, tsiku loyamba la mwezi waciwiri, caka caciwiri ataturuka m'dziko la Aigupto, ndi kuti, 2Werenga khamu lonse la ana a Israyeli, monga mwa mabanja ao, monga mwa nyumba ya makolo ao ndi kuwerenga maina ao, amuna onse mmodzi mmodzi. 3Iwe ndi Aroni muwawerenge monga mwa magulu ao, onse m'Israyeli akuturuka kunkhondo, kuyambira a zaka makumi awiri ndi mphambu, 4Ndipo pamodzi ndi inu pakhale munthu mmodzi wa mapfuko onse; yense mkuru wa nyumba ya kholo lace. 5Ndipo maina a amuna amene aime nanu ndi awa: wa Rubeni, Elizuri mwana wa Sedeuri. 6Wa Simeoni, Selumiyeli mwana wa Zurisadai. 7Wa Yuda, Nahesoni mwana wa Aminadabu. 8Wa Isakara, Netaneli mwana wa Zuwara. 9Wa Zebuloni, Eliyabu mwana wa Heloni. 10Wa ana a Yosefe: wa Efraimu, Elisama mwana wa Amihudi; wa Manase, Gamaliyeli mwana wa Pedazuri. 11Wa Benjamini, Abidana mwana wa Gideoni. 12Wa Dani, Ahiyezeri mwana wa Amisadai. 13Wa Aseri, Pagiyeli mwana wa Okirani. 14Wa Gadi, Eliyasafe mwana wa Deyueli. 15Wa Nafitali, Ahira mwana wa Enani. 16Iwo ndiwo oitanidwa a khamu, akalonga a mapfuko a makolo ao; ndiwo akuru a zikwizo za Israyeli. 17Ndipo Mose ndi Aroni anatenga anthu awa, onenedwa maina ao; 18nasonkhanitsa khamu lonse tsiku loyamba la mwezi waciwiri, ndipo iwo anawakumbira magwero ao kuchula mabanja ao, ndi nyumba za makolo ao, ndi kuwerenga maina kuyambira a zaka makumi awiri ndi mphambu mmodzi mmodzi. 19Monga Yehova anauza Mose, momwemo anawawerenga m'cipululu ca Sinai.

20Ndipo ana a Rubeni, mwana woyamba wa Israyeli, kubadwa kwao, monga mwa mabanja ao, monga mwa nyumba za makolo ao, powerenga maina mmodzi mmodzi, amuna onse kuyambira a zaka makumi awiri ndi mphambu, onse akuturukira kunkhondo; 21owerengedwa ao a pfuko la Rubeni, ndiwo zikwi makumi anai mphambu zisanu ndi cimodzi kudza mazana asanu.

22A ana a Simeoni, kubadwa kwao, monga mwa mabanja ao, monga mwa nyumba za makolo ao, owerengedwa ao, powerenga maina mmodzi mmodzi, amuna onse kuyambira a zaka makumi awiri ndi mphambu, onse akuturukira kunkhondo; 23owerengedwa ao a pfuko la Simeoni, ndiwo zikwi makumi asanu mphambu zisanu ndi zinai kudza mazana atatu.

24A ana a Gadi, kubadwa kwao, monga mwa mabanja ao, monga mwa nyumba za makolo ao, powerenga maina, kuyambira a zaka makumi awiri ndi mphambu, onse akuturukira kunkhondo; 25owerengedwa ao a pfuko la Gadi, ndiwo zikwi makumi anai mphambu zisanu kudza mazana asanu ndi limodzi mphambu makumi asanu.

26A ana a Yuda, kubadwa kwao, monga mwa mabanja ao, monga mwa nyumba za makolo ao, powerenga maina, kuyambira a zaka makomi awiri ndi mphambu, onse akuturukira kunkhondo; 27owerengedwa ao a pfuko la Yuda, ndiwo zikwi makumi asanu ndi awiri mphambu zinai kudza mazana asanu ndi limodzi.

28A ana a Isakara, kubadwa kwao, monga mwa mabanja ao, monga mwa nyumba za makolo ao, powerenga maina, kuyambira a zaka makumi awiri ndi mphambu, onse akuturukira kunkhondo; 29owerengedwa ao a pfuko la lsakara, ndiwo zikwi makumi asanu mphambu zinai kudza mazana anai.

30A ana a Zebuloni, kubadwa kwao, monga mwa mabanja ao, monga mwa
nyumba za makolo ao, powerenga maina, kuyambira a zaka makumi awiri ndi
mphambu, onse akuturukira kunkhondo; 31owerengedwa ao a pfuko la
Zebuloni, ndiwo zikwi makumi asanu mphambu zisanu ndi ziwiri kudza
mazana anai.
32A ana a Yosefe, ndiwo a ana a Efraimu, kubadwa kwao, monga mwa
mabanja ao, monga mwa nyumba za makolo ao, powerenga maina,
kuyambira a zaka makumi awiri ndi mphambu, onse akuturukira
kunkhondo; 33owerengedwa ao a pfuko la Efraimu, ndiwo zikwi makumi anai
mphambu mazana asanu.
34A ana a Manase, kubadwa kwao, monga mwa mabanja ao, monga mwa
nyumba za makolo ao, powerenga maina, kuyambira a zaka makumi awiri ndi
mphambu, onse akuturukira kunkhondo; 35owerengedwa ao a pfuko la
Manase, ndiwo zikwi makumi atatu mphambu ziwiri kudza mazana awiri.
36A ana a Benjamini, kubadwa kwao, monga mwa mabanja ao, monga mwa
nyumba za makolo ao, powerenga maina, kuyambira a zaka makumi awiri ndi
mphambu, onse akuturukira kunkhondo; 37owerengedwa ao a pfuko la
Benjamini, ndiwo zikwi makumi atatu mphambu zisanu kudza mazana anai.
38A ana a Dani, kubadwa kwao, monga mwa mabanja ao, monga mwa
nyumba za makolo ao, powerenga maina, kuyambira a zaka makumi awiri ndi
mphambu, onse akuturukira kunkhondo; 39owerengedwa ao a pfuko la Dani,
ndiwo zikwi makumi asanu ndi limodzi mphambu ziwiri kudza mazana asanu
ndi awiri.
40A ana a Aseri, kubadwa kwao, monga mwa mabanja ao, monga mwa
nyumba za makolo ao, powerenga maina, kuyambira a zaka makumi awiri ndi
mphambu, onse akuturukira kunkhondo; 41owerengedwa ao a pfuko la Aseri,
ndiwo zikwi makumi anai mphambu cimodzi kudza mazana asanu.
42A ana a Nafitali, kubadwa kwao, monga mwa mabanja ao, monga mwa
nyumba za makolo ao, powerenga maina, kuyambira a zaka makumi awiri ndi
mphambu, onse akuturukira kunkhondo; 43owerengedwa ao a pfuko la
Nafitali, ndiwo zikwi makumi asanu mphambu zitatu kudza mazana anai.
44Iwo ndiwo amene anawerengedwa, amene Mose anawerenga pamodzi ndi
Aroni, ndi akalonga a Israyeli, ndiwo amuna khumi ndi awiri; yense kunenera
nyumba ya kholo lace. 45Potero owerengedwa onse a ana a Israyeli monga
mwa nyumba za makolo ao, kuyambira a zaka makumi awiri ndi mphambu,
onse akuturukira kunkhondo m'Israyeli; 46inde owerengedwa onse ndiwo zikwi
mazana asanu ndi limodzi mphambu zitatu kudza mazana asanu ndi makumi
asanu.

Alevi sawerengedwa

47Koma Alevi monga mwa pfuko la makolo ao sanawerengedwa mwa
iwo. 48Popeza Yehova adalankhula ndi Mose, ndi kuti, 49Pfuko la Levi lokha
usaliwerenge, kapena kuona kufikira kwao mwa ana a Israyeli; 50koma iwe,
uike Alevi asunge kacisi wa mboni, ndi zipangizo zace zonse, ndi zonse ali
nazo; azinyamula kacisi, ndi zipangizo zace zonse; namtumikire, namange
mahema ao pozungulira pa kacisi. 51Ndipo akati amuke naye kacisiyo,
Aleviamgwetse, ndipo akati ammange, Alevi amuimike; ndipo mlendo
akayandikizako amuphe, 52Ndipo ana a Israyeli amange mahema ao, yense
ku cigono cace, ndi yense ku mbendera yace, monga mwa makamu
ao. 53Koma Alevi amange mahema ao pozungulira pa kacisi wa mboni, kuti
mkwiyo ungagwere khamu la ana a Israyeli; ndipo Alevi azidikira kacisi wa
mboni. 54Momwemo ana a Israyeli anacita monga mwa zonse Yehova adauza
Mosel anacita momwemo.

Malongosoledwe a cigono

1Ndipo Yehova ananena ndi Mose ndi Aroni, nati, 2Ana a Israyeli
azimanga mahema ao yense ku mbendera yace, ya cizindikilo ca
nyumba ya kholo lace; amange mahema ao popenyana ndi cihema
cokomanako pozungulira. 3Ndipo iwo akumanga mahema ao ku
m'mawa koturuka dzuwa ndiwo a mbendera ya cigono ca Yuda,
monga mwa makamu ao; ndipo kalonga wa ana a Yuda ndiye
Nahesoni mwana wa Aminadabu. 4Ndipo khamu lace, ndi
owerengedwa ao, ndiwo zikwi makumi asanu ndi awiri, mphambu
zinai, kudza mazana asanu ndi limodzi. 5Ndipo iwo akumanga
mahema ao poyandikizana naye ndiwo a pfuko la Isakara; ndipo
kalonga wa ana a Isakara ndiye Netandi mwana wa Zuwara. 6Ndipo
khamu lace, ndi owerengedwa ace, ndiwo zikwi makumi asanu
mphambu zinai kudza mazana anai. 7Ndi pfuko la Zebuloni:
kalonga wa ana a Zebuloni ndiye Eliyabu mwana wa Heloni. 8Ndi
khamu lace, ndi owerengedwa ace, ndiwo zikwi makumi asanu
mphambu zisanu ndi ziwiri kudza mazana anai. 9Owerengedwa
onse a cigono ca Yuda ndiwo zikwi makumi khumi mphambu
makumi asanu ndi atatu kudza zisanu ndi cimodzi mphambu
mazana anai, monga mwa makamu ao, Ndiwo azitsogolera ulendo.
10Mbendera ya cigono ca Rubeni ikhale kumwera monga mwa
makamu ao; ndipo kalonga wa ana a Rubeni ndiye Elizuri mwana
wa Sedeuri. 11Ndi khamu lace, ndi olembedwa ace, ndiwo zikwi
makumi anai mphambu zisanu ndi cimodzi kudza mazana
asanu. 12Ndipo iwo akumanga mahema ao poyandikizana naye
ndiwo a pfuko la Simeoni; ndi kalonga wa ana a Simeoni ndiye
Selumiyeli mwana wa Surisadai. 13Ndi khamu lace ndi
owerengedwa ace, ndiwo zikwi makumi asanu mphambu zisanu
ndi zinai kudza mazana atatu. 14Ndi pfuko la Gadi; kalonga wa ana
a Gadi ndiye Eliyasafe mwana wa Reueli. 15Ndi khamu lace, ndi
owerengedwa ace, ndiwo zikwi makumi anai mphambu zisanu
kudza mazana asanu ndi limodzi mphambu makumi
asanu. 16Owerengedwa onse a cigono ca Rubeni ndiwo zikwi
makumi khumi mphambu makumi asanu ndi cimodzi kudza
mazana anai mphambu makumi asanu, monga mwa makamu ao.
Ndiwo azitsatana nao otsogolerawo.
17Pamenepo khamu la Alevi azimuka naco cihema cokomanako,
pakati pa makamu; monga amamanga mahema ao, momwemo
azimuka ulendo wao, munthu yense pamalo pace, monga mwa
mbendera zao.
18Mbendera ya cigono ca Efraimu izikhala kumadzulo monga mwa
makamu ao; ndipo kalonga wa ana a Efraimu ndiye Elisama
mwana wa Amihudi. 19Ndi khamu lace, ndi owerengedwa ace,

ndiwo zikwi makumi anai kudza mazana asanu. 20Ndipo
oyandikizana naye ndiwo a pfuko la Manase; ndi kalonga wa ana a
Manase ndiye Gamaliyeli mwana wa Pedazuri. 21Ndi khamu lace,
ndi owerengedwa ace, ndiwo zikwi makumi atatu mphambu ziwiri
kudza mazana awiri. 22Ndi pfuko la Benjamini: kalonga wa ana a
Benjamini ndiye Abidana mwana wa Gideoni. 23Ndi khamu lace,
ndi owerengedwa ace, ndiwo zikwi makumi atatu mphambu zisanu
kudza mazana anai. 24Owerengedwa onse a cigono ca Efraimu
ndiwo zikwi makumi khumi mphambu zisanu ndi zitatu kudza zana
limodzi, monga mwa makamu ao. Iwo ndiwo aziyenda gulu lacitatu
paulendo.
25Mbendera ya cigono ca Dani izikhala kumpoto monga mwa
makamu ao; ndi kalonga wa ana a Dani ndiye Ahiyezeri mwana wa
Amisadai. 26Ndi khamu lace, ndi owerengedwa ace, ndiwo zikwi
makumi asanu ndi limodzi mphambu ziwiri kudza mazana asanu
ndi awiri. 27Ndipo iwo akumanga mahema ao poyandikizana naye
ndiwo a pfuko la Aseri; ndi kalonga wa ana a Aseri ndiye Pagiyeli
mwana wa Okirani. 28Ndi khamu lace, ndi owerengedwa ace, ndiwo
zikwi makumi anai mphambu cimodzi kudza mazana asanu. 29Ndi
pfuko la Nafitali: ndi kalonga wa ana a Nafitali ndiye Ahira mwana
wa Enani. 30Ndi khamu lace, ndi owerengedwa ace, ndiwo zikwi
makumi asanu mphambu zitatu kudza mazana
anai. 31Owerengedwa onse a cigono ca Dani ndiwo zikwi makumi
khumi mphambu makumi asanu kudza zisanu ndi ziwiri mphambu
mazana asanu ndi Hmodzi. Iwo ndiwo aziyenda m'mbuyo
paulendo, monga mwa mbendera zao.
32Amenewo ndiwo anawerengedwa a ana a Israyeli monga mwa
nyumba za makolo ao; owerengedwa onse a m'zigono, monga
mwa makamu ao, ndiwo zikwi makumi khumi kasanu ndi kamodzi
mphambu zitatu kudza mazana asanu ndi makumi asanu. 33Koma
sanawerenga Alevi mwa ana a Israyeli; monga Yehova adauza
Mose. 34Ndipo ana a Israyeli anacita monga mwa zonse Yehova
adauza Mose, momwemo anamanga mahema ao pa mbendera
zao, momwemonso anayenda paulendo, yense monga mwa
mabanja ace, monga mwa nyumba za makolo ace.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Nchito ya Alevi

1Mibadwo ya Aroni ndi Mose, tsiku lija Yehova ananena ndi Mose
m'phiri la Sinai, ndi iyo. 2Ndipo maina ao a ana amuna a Aroni ndi
awa: Woyamba Nadabu, ndi Abihu, Eleazara, ndi Itamara. 3Awa ndi
maina a ana amuna a Aroni, ansembe odzozedwawo, amene
anawadzaza manja ao acite nchito ya nsembe. 4Koma Nadabu ndi
Abihu anafa pamaso pa Yehova muja anabwera nao moto
wacilendo pamaso pa Yehova, m'cipululu ca Sinai, ndipo analibe
ana; koma Eleazara ndi Itamara anacita Debito ya nsembe pamaso
pa atate wao Aroni.
5Ndipo Yehova ananena ndi Mose, nati, 6Sendera nalo kuno pfuko
la Levi, ndi kuwaika pamaso pa Aroni wansembe, kuti
amtumikire. 7Ndipo azisunga udikiro wace, ndi udikiro wa khamu
lonse pa khomo la cihema cokomanako, kucita nchito ya
kacisi. 8Ndipo asunge zipangizo zonse za cihema cokomanako, ndi
udikiro wa ana a Israyeli, kuicita nchito ya kacisi. 9Ndipo uzipereka
Alevi kwa Aroni ndi kwa ana ace amuna; apatsidwa kwa iye ndithu,
ocokera kwa ana a Israyeli. 10Koma uike Aroni ndi ana ace amuna,
azisunga nchito yao ya nsembe; ndi mlendo wakusendera pafupi
amuphe.
11Ndipo Yehova ananena ndi Mose, nati, 12Ndipo taonani, Ine
ndatenga Alevi kuwacotsa pakati pa ana a Israyeli m'malo mwa
ana ovamba onse, oyamba kubadwa mwa ana a Israyeli; ndipo
Aleviwo ndi anga. 13Pakuti ana oyamba onse ndi anga; tsiku lija
ndinakantha ana oyamba onse m'dziko la Aigupto ndinadzipatulira
ana oyamba onse m'Israyeli, kuyambira munthu kufikira coweta;
ndiwo anga; Ine ndine Yehova.
14Ndipo Yehova ananena ndi Mose m'cipululu ca Sinai,
nati, 15Werenga ana a Levi monga mwa nyumba ya makolo ao,
monga mwa mabanja ao; uwawerenge mwamuna yense wa mwezi
umodzi ndi mphambu. 16Ndipo Mose anawawerenga monga mwa
mau a Yehova, monga adamuuza. 17Ndipo ana a Levi maina ao ndi
awa: Gerisoni, ndi Kohati ndi Merari. 18Ndi ana a Gerisoni maina ao
ndi awa, monga mwa mabanja ao: Libini, ndi Simei. 19Ndi ana a
Kohati monga mwa mabanja ao: Amiramu ndi Izara, Hebroni ndi
Uziyeli. 20Ndi ana a Merari monga mwa mabanja ao: Mali ndi Musi.
Awa ndi mabanja a Alevi monga mwa nyumba za makolo ao.
21Banja la Libini, ndi mabanja a Simei, ndiwo a Gerisoni; ndiwo
mabanja a Gerisoni. 22Owerengedwa ao, powawerenga amuna
onse, kuyambira mwana wa mwezi umodzi ndi mphambu,
owerengedwa ao ndiwo zikwi zisanu ndi ziwiri mphambu mazana
asanu. 23Mabanja a Agerisoni azimanga mahema ao pambuyo pa
kacisi kumadzulo. 24Ndipo kalonga wa nyumba ya makolo a

Agerisoni ndiye Eliyasafe mwana wa Layeli. 25Ndipo udikiro wa ana a Gerisoni m'cihema cokomanako ndiwo kacisi, ndi cihema, cophimba cace, ndi nsaru yotsekera pa khomo la cihema cokomanako, 26ndi nsaru zocinga za kubwalo, ndi nsaru yotsekera pa cipata ca pabwalo, lokhala kukacisi, ndi ku guwa la nsembe pozungulira, ndi zingwe zace za ku nchito zace zonse.
27Banja la Aamiramu, ndi banja la Aizara, ndi banja la Ahebroni, ndi banja la Auziyeli ndiwo a Kohati; ndiwo mabanja a Akohati. 28Powawerenga amuna onse, kuyambira a mwezi umodzi ndi mphambu ndiwo zikwi zisanu ndi zitatu mphambu mazana asanu ndi limodzi, akusunga udikiro wa pa malo opatulika. 29Mabanja a ana a Kohati azimanga mahema ao pa mbali ya kacisi ya kumwera. 30Ndipo kalonga wa nyumba ya makolo ao ya mabanja a Akohati ndiye Elizafana mwana wa Uziyeli. 31Ndipoudikirowaondiwo likasa, ndi gome, ndi coikapo nyali, ndimagome a nsembe, ndi zipangizo za malo opatulika zimene acita nazo, ndi nsaru yocinga, ndi nchito zace zonse. 32Ndipo kalonga wa akalonga a Alevi ndiye Eleazara mwana wa Aroni wansembeyo; ndiye aziyang'anira osunga udikiro wa pa malo opatulika.
33Banja la Amali, ndi banja la Amusi ndiwo a Merari; ndiwo mabanja a Merari. 34Ndipo owerengedwa ao, powerenga amuna onse, kuyambira a mwezi umodzi ndi mphambu, ndiwo zikwi zisanu ndi cimodzi kudza mazana awiri. 35Ndi kalonga wa nyumba ya makolo ya mabanja a Merari ndiye Zuriyeli mwana wa Abiyaili; azimanga mahema ao pa mbali ya kacisi ya kumpoto. 36Ndipo coyang'anira iwo, udikiro wao wa ana a Merari ndiwo matabwa a kacisi, ndi mitanda yace, ndi mizati ndi nsanamira zace, ndi makamwa ace, ndi zipangizo zace zonse, ndi nchito zace zonse; 37ndi nsici za pabwalo pozungulira, ndi makamwa ace, ndi ziciri zace, ndi zingwe zace. 38Ndipo amene adamanga mahema ao pa khomo la kacisi, kum'mawa, pa khomo la cihema cokomanako koturukira dzuwa, ndiwo Mose ndi Aroni, ndi ana ace amuna, akusunga udikiro wa malo opatulika, ndiwo udikiro wa ana a Israyeli; koma mlendo wakuyandikizako amuphe, 39Owerengedwa onse a Alevi, adawawerenga Mose ndi Aroni, powauza Yehova, monga mwa mabanja ao, amuna onse kuyambira a mwezi umodzi ndi mphambu, ndiwo zikwi makumi awiri mphambu ziwiri.
40Ndipo Yehova anati kwa Mose, Werenga amuna oyamba kubadwa onse a ana a Israyeli kuyambira a mwezi umodzi ndi mphambu nuone ciwerengo ca maina ao. 41Ndipo unditengere Ine Alevi (ine ndine Yehova) m'malo mwa oyamba kubadwa onse mwa ana a Israyeli; ndi ng'ombe za Alevi m'malo mwa zoyamba kubadwa zonse mwa ng'ombe za ana a Israyeli. 42Ndipo Mose

anawawerenga, monga Yehova adamuuza, oyamba kubadwa onse
mwa ana a Israyeli. 43Ndipo amuna onse oyamba kubadwa,
powerenga maina, kuyambira a mwezi umodzi ndi mphambu,
owerengedwa ao, ndiwo zikwi makumi awiri mphambu ziwiri kudza
mazana awiri ndi makumi asanu ndi awiri mphambu atatu.
44Ndipo Yehova ananena ndi Mose, nati, 45Landira Alevi m'malo
mwa oyamba kubadwa onse mwa ana a Israyeli, ndi ng'ombe za
Alevi m'malo mwa ng'ombe zao; ndipo Alevi azikhala anga; Ine
ndine Yehova. 46Kunena za mazana awiri ndi makumi asanu ndi
awiri kudza atatuwo oyamba kubadwa a ana a Israyeli, akuposa
Alevi, akaomboledwe, 47ulandire masekeli asanu pa munthu
mmodzi; uwalandire pa muyeso wa sekeli wa malo opatulika
(sekeli ndiwo magera makumi awiri); 48nupereke ndarama zimene
akuposawo anaomboledwa nazo kwa Aroni ndi kwa ana ace
amuna. 49Pamenepo Mose analandira ndarama zaom bola nazo
kwa iwo akuposa aja adawaombola Alevi; 50analandira ndaramazo
kwa oyamba kubadwa a ana a Israyeli; masekeli cikwi cimodzi
mphambu mazana atatu kudza makumi asanu ndi limodzi
mphambu asanu, kuyesa sekeli wa malo opatulika. 51Ndipo Mose
anapatsa Aroni ndi ana ace ndarama zaom bola nazo monga mwa
mau a Yehova, monga Yehova adauza Mose.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Akohati

1Ndipo Yehova ananena ndi Mose ndi Aroni, nati, 2Werengani ana a Kohati
pakati pa ana a Levi, monga mwa mabanja ao, monga mwa nyumba za
makolo ao, 3kuyambira a zaka makumi atatu ndi mphambu, kufikira zaka
makumi asanu, onse akulowa utumikiwu, kuti agwire nchito ya cihema
cokomanako. 4Nchito ya ana a Kohati m'cihema cokomanako ndi iyi, kunena
za zinthu zopatulikitsa: 5akati amuke a m'cigono, Aroni ndi ana ace amuna
azilowa, natsitse nsaru yocinga, ndi kuphimba nayo likasa la mboni, 6ndi
kuikapo cophimba ca zikopa za akatumbu; ndi kuyalapo nsaru yamadzi yeni
yeni, ndi kupisako mphiko zace. 7Ndi pa gome la mkate waonekera ayale
nsaru yamadzi, naikepo mbale zace, ndi zipande, ndi mitsuko, ndi zikho
zakuthira nazo; mkate wa cikhalire uzikhalaponso. 8Ndipo ayale pa izi nsaru
yofiira, ndi kuliphimba ndi cophimba ca zikopa za akatumbu, ndi kupisako
mphiko zace. 9Ndipo atenge nsaru yamadzi, ndi kuphimba coikapo nyali
younikira, ndi nyali zace, ndi mbano zace, ndi zaolera zace, ndi zotengera
zace zonse za mafuta zogwira nazo nchito yace. 10Ndipo acimange ndi
cipangizo zace zonse m'cophimba ca zikopa za akatumbu, ndi kuziika pa
conyamulira. 11Ndipo pa guwa la nsembe lagolidi aziyala nsaru yamadzi,
naliphimbe ndi cophimba ca zikopa za akatumbu, ndi kupisako mphiko
zace. 12Natenge zipangizo zace zonse za utumiki, zimene atumikira nazo
m'malo opatulika, nazimange m'nsaru yamadzi, ndi kuziphimba ndi cophimba
ca zikopa za akatumbu, ndi kuziika paconyamulira. 13Ndipo azicotsa mapulusa
pa guwa la nsembe, ndi kuyala pa ilo nsaru yofiirira. 14Naikepo zipangizo zace
zonse, zimene atumikira nazo pamenepo, mbale za zofukiza, mitungo, ndi
zaolera, ndi mbale zowazira, zipangizo zonse za guwa la nsembe; nayalepo
cophimba ca zikopa za akatumbu, ndi kupisako mphiko zace. 15Atatha Aroni
ndi ana ace amuna kuphimba malo opatulika, ndi zipangizo zace zonse za
malo opatulika, pofuna kumuka am'cigono; atatero, ana a Kohati adze
kuzinyamula; koma asakhudze zopatulikazo, kuti angafe. Zinthu izi ndizo
akatundu a ana a Kohati m'cihema cokomanako. 16Ndipo zoyang'anira
Eleazara, mwana wa Aroni wansembe, ndizo mafuta a nyaliyo, ndi cofukiza ca
pfungo lokoma, ndi nsembe yaufa kosalekeza, ndi mafuta odzoza, udikiro wa
kacisi wonse, ndi zonse ziri m'mwemo, malo opatulika, ndi zipangizo zace.
17Ndipo Yehova ananena ndi Mose ndi Aroni, Dati, 18Musamasadza pfuko la
mabanja a Kohati kuwacotsa pakati pa Alevi; 19koma muzitero nao kuti akhale
ndi moyo, osafa ai, poyandikiza iwo zopatulikitsazo; Aroni ndi ana ace amuna
alowe, namuikire munthu yense nchito yace ndi katundu wace. 20Koma
asalowe kukaona zopatulikazo pozikulunga, kuti angafe.

Agerisoni

21Ndipo Yehova ananena ndi Mose, nati, 22Werenganso ana a Gerisoni, monga
mwa nyumba za makolo ao, monga mwa mabanja ao. 23Uwawerenge
kuyambira a zaka makumi atatu ndi mphambu, kufikira a zaka makumi asanu;
onse akulowa kutumikira utumikiwo, kucita nchitoyi m'cihema
cokomanako. 24Nchito ya mabanja a Agerisoni, pogwira nchito ndi kusenza
katundu ndi iyi; 25azinyamula nsaru zophimba za kacisi, ndi cihema
cokomanako, cophimba cace, ndi cophimba ca zikopa za akatumbu ciri
pamwamba pace, ndi nsaru yotsekera pa khomo la cihema
cokomanako; 26ndi nsaru zocingira za pabwalo, ndi nsaru yotsekera ku cipata
ca pabwalo liri pakacisi ndi pa guwa la nsembe pozungulira, ndi zingwe zao,
ndi zipangizo zonse za Debito zao, ndi zonse acita nazo; m'menemo muli
nchito zao. 27Nchito yonse ya ana a Agerisoni, kunena za akatundu ao ndi

nchito zao zonse, ikhale monga adzanena Aroni ndi ana ace amuna; ndipo muwaike adikire akatundu ao onse. 28Iyi ndi nchito ya mabanja a ana a Gerisoni m'cihema cokomanako; ndipo Itamara mwana wa Aroni wansembe ayang'anire udikiro wao.

Amerari

29Kunena za ana a Merari, Uwawerenge monga mwa mabanja ao, monga mwa nyumba za makolo ao. 30Uwawerenge kuyambira a zaka makumi atatu ndi mphambu kufikira a zaka makumi asanu, onse akulowa utumikiwu, kucita nchito ya cihema cokomanako. 31Ndipo udikiro wa akatundu ao, monga mwa nchito zao zonse m'cihema cokomanako ndi ici: matabwa a kacisi, ndi mitanda yace, ndi mizati ndi nsanamira zace, ndi makamwa ace; 32ndi nsici za kubwalo kozungulira, ndi makamwa ace, ndi ziciri zace, ndi zingwe zace, pamodzi ndi zipangizo zace zonse, ndi nchito yace yonse; ndipo muziwerenga zipangizo za udikiro wa akatundu ao ndi kuwaehula maina ao. 33Iyi ndi nchito ya mabanja a ana a Merari, monga mwa nchito zao zonse m'cihema cokomanako, mowauza Itamara mwana wa Aroni wansembe.

34Ndipo Mose ndi Aroni ndi akalonga a khamu anawerenga ana a Akohati monga mwa mabanja ao, ndi monga mwa nyumba za makolo ao, 35kuyambira a zaka makumi atatu ndi mphambu kufikira a zaka makumi asanu, onse akulowa utumikiwu, kuti agwire Debito m'cihema cokomanako; 36ndipo owerengedwa ao monga mwa mabanja ao ndiwo zikwi ziwiri mphambu mazana asanu ndi awiri kudza makumi asanu. 37Awa ndi owerengedwa a mabanja a Akohati, onse akutumikira m'cihema cokomanako, amene Mose ndi Aroni anawawerenga monga mwa mau a Yehova mwa dzanja la Mose.

38Ndipo ana owerengedwa a Gerisoni, monga mwa mabanja ao, ndi monga mwa nyu mba za makolo ao, 39kuyambira a zaka makumi atatu ndi mphambu kufikira a zaka makumi asanu, onse akulowa utumikiwu, kuti agwire nchito m'cihema cokomanako, 40owerengedwa ao, monga mwa mabanja ao, monga mwa nyumba za makolo ao, ndiwo zikwi ziwiri mphambu mazana asanu ndi limodzi kudza makumi atatu. 41Amenewo ndiwo owerengedwa a mabanja a ana a Gerisoni, onse akutumikira m'cihema cokomanako, adawawerenga Mose ndi Aroni monga mwa mau a Yehova.

42Ndipo owerengedwa a mabanja a ana a Merari, monga mwa mabanja ao, monga mwa nyumba za makolo ao, 43kuyambira a zaka makumi atatu ndi mphambu kufikira a zaka makumi asanu, onse akulowa utumikiwu kuti agwire nchito m'cihema cokomanako, 44owerengedwa ao monga mwa mabanja ao, ndiwo zikwi zitatu ndi mazana awiri. 45Amenewo ndiwo owerengedwa a mabanja a ana a Merari, amene Mose ndi Aroni anawawerenga monga mwa mau a Yehova mwa dzanja la Mose.

Kuwerengedwa kwa Alevi

46Owerengedwa onse a Alevi, amene Mose ndi Aroni ndi akalonga a Israyeli anawawerengera, monga mwa mabanja ao, ndi monga mwa nyumba za makolo ao, 47kuyambira a zaka makumi atatu ndi mphambu kufikira a zaka makumi asanu, onse akulowa kugwira nchito ya utumikiwu, ndiyo nchito ya akatundu m'cihema cokomanako; 48owerengedwa ao ndiwo zikwi zisanu ndi zitatu kudza mazana asanu mphambu makumi asanu ndi atatu. 49Anawawerenga monga mwa mau a Yehova ndi dzanja la Mose, onse monga mwa nchito zao, ndi monga mwa akatundu ao; anawawerenga monga momwe Yehova adauza Mose.

Odetsedwa onse acotsedwe kucigono

1Ndipo Yehova ananena ndi Mose, ndi kuti, 2Uza ana a Israyeli kuti aziturutsa m'cigono akhate onse, ndi onse akukhala nako kukha, ndi onse odetsedwa cifukwa ca akufa; 3muwaturutse amuna ndi akazi muwaturutsire kunja kwa cigono, kuti angadetse cigono cao, cimene ndikhala m'kati mwacemo. 4Ndipo ana a Israyeli anacita cotero, nawaturutsira kunja kwa cigono; monga Yehova adanena ndi Mose momwemo ana a Israyeli anacita.

Za Kubwezera

5Ndipo Yehova ananena ndi Mose, nati, 6Nena ndi ana a Israyeli, ndi kuti, Mwamuna kapena mkazi akacita cimo liri lonse amacita anthu, kucita mosakhulupirika pa Yehova, nakaparamuladi; 7azibvomereza cimo lace adalicita; nabwezere coparamulaco monsemo, naonjezeko limodzi la magawo asanu, ndi kucipereka kwa iye adamparamulayo. 8Koma munthuyo akapanda kukhala nayo nkhoswe imene akaibwezere coparamulaco, coparamula acibwezera Yehovaco cikhale ca wansembe; pamodzi ndi nkhosa yamphongo ya cotetezerapo, imene amcitire nayo comtetezera. 9Ndipo nsembe zokweza zonse za zinthu zopatulika za ana a Israyeli, zimene abwera nazo kwa wansembe zisanduka zace. 10Zopatulika za munthu ali yense ndi zace: ziti zonse munthu ali yense akapatsa wansembe, zasanduka zace.

Za mlandu wa nsanje

11Ndipo Yehova ananena ndi Mose, nati, 12Nena ndi ana a Israyeli, nuti nao, Mkazi wa mwini akapatukira mwamuna wace, nakamcitira mosakhulupirika, 13ndi munthu akagona naye, koma kumbisikira maso a mwamuna wace, ndikumng'unira; nadetsedwa mkaziyo, koma palibe mboni yomtsutsa, kapena sanamgwira alimkucita; 14ndipo ukamgwira mwamuna mtima wansanje, kuti acitire nsanje mkazi wace, popeza wadetsedwa; kapena ukamgwira mtima wansanje, kuti amcitire mkazi wace nsanje angakhale sanadetsedwa; 15pamenepo mwamunayo azidza naye mkazi wace kwa wansembe, nadze naco copereka cace, limodzi la magawo khumi la efa wa ufa wabarele; asathirepo mafuta, kapena kuikapo libano; popeza ndiyo nsembe yaufa yansanje, nsembe yaufa yacikumbutso, yakukumbutsa mphulupulu. 16Ndipo wansembe abwere naye, namuike pamaso pa Yehova; 17natenge madzi opatulika m'mbale yadothi wansembeyo, natengeko pfumbi liri pansi m'kacisi, wansembeyo nalithire m'madzimo. 18Pamenepo wansembeyo aike mkaziyo pamaso pa Mulungu, nabvula mutu wa mkaziyo, naike nsembe yaufa yacikumbutso m'manja mwace, ndiyo nsembe yaufa yansanje; ndipo m'manja mwace mwa wansembe muzikhala madzi owawa akudzetsa temberero. 19Ndipo

wansembe amlumbiritse, nanene kwa mkazi, Ngati sanagona nawe munthu mmodzi yense, ngati sunapatukira kucidetso, pokhala ndiwe wa mwamuna wako, upulumuke ku madzi owawa awa akudzetsa temberero. 20Koma iwe, ngati wapatukira mwamuna wako, ngati wadetsedwa, kuti wagona nawe munthu, wosati mwamuna wako; 21pamenepo wansembe alumbiritse mkazi lumbiro lakutemberera, ndi wansembe anene kwa mkazi, Yehova akuike ukhale temberero ndi lumbiro pakati pa anthu a mtundu wako, pakuondetsa Yehova m'cuuno mwako, ndi kukutupitsa mbulu; 22ndipo madzi awa akudzetsa temberero adzalowa m'matumbo mwako, nadzakutupitsa mbulu ndi kuondetsa m'cuuno mwako; ndipo mkaziyo aziti, Amen, Amen. 23Ndipo wansembe alembere matemberero awa m'buku, ndi kuwafafaniza ndi madzi owawawa. 24Ndipo amwetse mkaziyo madzi owawa akudzetsa temberero; ndi madzi odzetsa temberero adzalowa mwa iye nadzamwawira. 25Ndipo wansembe atenge nsembe yaufa m'manja mwa mkazi, naweyule nsembe yaufa pamaso pa Yehova, nabwere nayo ku guwa la nsembe. 26Wansembe atengekonso nsembe yaufa wodzala manja, cikumbutso cace, nacitenthe pa guwa la nsembe; ndipo atatero amwetse mkazi madziwo. 27Ndipo atammwetsa madziwo, kudzatero, ngati wadetsedwa, nacita mosakhulupitika pa mwamuna wace, madzi odzetsa tembererowo adzalowa mwa iye nadzamwawira, nadzamtupitsa mbulu, ndi m'cuuno mwace mudzaonda; ndi mkaziyo adzakhala temberero pakati pa anthu a mtundu wace. 28Koma ngati mkazi sanadetsedwa, nakhala woyera, pamenepo adzapulumuka, nadzaima. 29Ici ndi cilamulo ca nsanje, pamene mkazi, pokhala naye mwamuna wace, ampatukira nadetsedwa; 30kapena pamene mtima wansanje umgwira mwamuna, ndipo acitira mkazi wace nsanje; pamenepo aziika mkazi pamaso pa Yehova, ndipo wansembe amcitire cilamulo ici conse. 31Mwamunayo ndiye wosacita mphulupulu, koma mkazi uyo asenze mphulupulu yace.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Za cowinda ca Mnaziri

1Ndipo Yehova ananena ndi Mose, nati, 2Nena ndi ana a Israyeli, nuti nao,
Mwamuna kapena mkazi akadzipatulira kulonieza cowinda ca Mnaziri,
kudzipatulira kwa Yehova; 3azisala vinyo ndi kacasu; asamwe vinyo wosasa,
kapena kacasu wosasa, kapena cakumwa conse ca mphesa, asamwe; asadye
mphesa zaziwisi kapena zouma. 4Masiku onse a kusala kwace asadye kanthu
kopangika ndi mphesa, kuyambira nthanga zace kufikira khungu lace, 5Masiku
onse a cowinda cace cakusala, lumo lisapite pamutu pace; kufikira adatha
masikuwo adadzipatulira kwa Yehova, azikhala wopatulika; aleke nzera za
tsitsi lace zimeretu. 6Masiku onse akudzipatulira kwa Yehova asayandikize
mtembo. 7Asadzidetse ndi atate wace, kapena mai wace, mbale wace, kapena
mlongo wace, akafa iwowa; popeza cowindira Mulungu wace ciri pamutu
pace. 8Masiku onse a kusala kwace akhala wopatulikira kwa Yehova. 9Munthu
akafa cikomo pali iye, ndipo akadetsa mutu wace wowinda; pamenepo
azimeta mutu wace tsiku la kumyeretsa kwace, tsiku lacisanu ndi ciwiri
aumete. 10Ndipo tsiku lacisanu ndi citato adze nazo njiwa ziwiri, kapena
maunda awiri, kwa wansembe, ku khomo la cihema cokomanako; 11ndipo
wansembe akonze imodzi nsembe yaucimo, ndi yina nsembe yopsereza,
namtetezere popeza anacimwa nao mtembowo; ndipo apatulire mutu wace
tsiku lomwelo. 12Ndipo awapatulire Yehova masiku a kusala kwace, nadze
nayo nkhosa yamphongo ya caka cimodzi ikhale nsembe yoparamula; koma
masiku adapitawa azikhala cabe, popeza anadetsa kusala kwace.
13Ndipo cilamulo ca Mnaziri, atatha masiku a kusala kwace ndi ici: azidza
naye ku khomo la cihema cokomanako; 14pamenepo abwere naco copereka
cace kwa Yehova, nkhosa yamphongo ya caka cimodzi yopanda cirema, ikhale
nsembe yopsereza, ndi nkhosa yamsoti yopanda cirema ikhale nsembe
yaucimo, ndi nkhosa yamphongo yopanda cirema ikhale nsembe
yoyamika; 15ndi mtanga wa mkate wopanda cotupitsa, timitanda ta ufa
wosalala tosanganiza ndi mafuta, ndi timitanda taphanthi todzoza ndi mafuta,
ndi nsembe yao yaufa, ndi nsembe zao zothira. 16Ndipo wansembe azibwera
nazo pamaso pa Yehova, nakonze nsembe yace yaucimo, ndi nsembe yace
yopsereza; 17naphe nkhosa yamphongo yoyamika ya Yehova, pamodzi ndi
mtanga wa mkate wopanda cotupitsa; wansembe akonzenso nsembe yace
yaufa, ndi nsembe yace yothira. 18Pamenepo Mnaziriyo amete mutu wace wa
kusala kwace pa khomo la cihema cokomanako, natenge tsitsi la pa mutu
wace wa kusala, naliike pamoto wokhala pansi pa nsembe yoyamika. 19Ndipo
wansembe atenge mwendo wamwamba wophika wa nkhosa yamphongo, ndi
kamtanda kamodzi kopanda cotupitsa ka m'mtanga, ndi kamtanda kaphanthi
kopanda cotupitsa kamodzi, ndi kuziika m'manja mwa Mnaziri, atameta kusala
kwace; 20ndipo wansembe aziweyula nsembe yoweyula pamaso pa Yehova;
ici ncopatulikira wansembe, pamodzi ndi nganga ya nsembe yoweyula,
pamodzi ndi mwendo wa nsembe yokweza; ndipo atatero Mnaziri amwe
vinyo. 21Ici ndi cilamulo ca Mnaziri wakuwinda, ndi ca copereka cace ca
Yehova cifukwa ca kusala kwace, pamodzi naco cimene dzanja lace likacipeza;
azicita monga mwa cowinda cace anaciwinda, mwa cilamulo ca kusala.

Mau a mdalitso

22Ndipo Yehova ananena ndi Mose, ndi kuti, 23Nena ndi Aroni ndi ana ace, ndi
kuti, Uzidalitsa ana a Israyeli motero; uziti nao,
24Yehova akudalitse iwe, nakusunge;
25Yehova awalitse nkhope yace pa iwe, nakucitire cisomo;
26Yehova akweze nkhope yace pa iwe, nakupatse mtendere.

27Potero aike dzina langa pa ana a Israyeli; ndipo ndidzawadalitsa.

Zopereka za Akuru 12 atautsa cihemaco

1Ndipo kunali kuti tsiku lomwe Mose anatsiriza kumuutsa kacisi,
namdzoza ndi kumpatula, ndi zipangizo zace zonse, ndi guwa la
nsembe, ndi zipangizo zace zonse, nazidzoza ndi
kuzipatula; 2akalonga a Israyeli, akuru a nyumba za makolo ao,
anapereka nsembe, ndiwo akalonga a mapfuko akuyang'anira
owerengedwa; 3anadza naco copereka cao pamaso pa Yehova,
magareta ophimbika asanu ndi mmodzi, ndi ng'ombe khumi ndi
ziwfri; akalonga awiri anapereka gareta mmodzi, ndi kalonga
mmodzi ng'ombe imodzi; nabwera nazo pakhomo pa kacisi. 4Ndipo
Yehova ananena ndi Mose, ndi kuti, 5Uzilandira kwa iwo, kuti
zikhale zakucitira nchito ya cihema cokomanako; nuzipereke kwa
Alevi, yense monga mwa nchito yace. 6Ndipo Mose analandira
magareta ndi ng'ombe, nazipereka kwa Alevi. 7Anapatsa ana a
Gerisoni magareta awiri ndi ng'ombe zinai, monga mwa nchito
yao; 8napatsa ana a Merari magareta anai ndi ng'ombe zisanu ndi
zitatu, monga mwa nchito yao; wakuziyang'anira ndiye Itamara
mwana wa Aroni wansembe. 9Koma sanapatsa ana a Kohati
kanthu; popeza nchito yao ndiyo ya zinthu zopatulika, zimene
amazisenza pa mapewa ao. 10Ndipo akalonga anabwera nazo za
kupereka ciperekere guwa la nsembe tsiku lodzozedwa ili; inde
akalongawo anabwera naco copereka cao pa guwa la
nsembelo. 11Ndipo Yehova ananena ndi Mose, Akalonga onse,
yense pa tsiku lace, apereke zopereka zao za kupereka ciperekere
guwa la nsembe.
12Wakubwera naco copereka cace tsiku loyamba ndiye Nahesoni
mwana wa Aminadabu, wa pfuko la Yuda: 13copereka cace ndico
mbizi imodzi yasiliva, kulemera kwace ndiko masekeli zana limodzi
ndi makumi atatu, mbale yowazira imodzi yasiliva ya masekeli
makumi asanu ndi awiri, kuyesa sekeli wa malo opatulika; zonse
ziwirizo zodzala ndi ufa wosalala wosanganiza ndi mafuta ukhale
nsembeyaufa; 14cipande cimodzi cagolidi ca masekeli khumi,
codzala ndi cofukiza; 15ng'ombe yamphongo imodzi, nkhosa
yamphongo imodzi, mwana wa nkhosa mmodzi wa caka cimodzi,
zikhale nsembe yopsereza; 16ronde mmodzi akhale nsembe
yaucimo; 17ndi nsembe yoyamika, ng'ombe ziwiri, nkhosa
zamphongo zisanu, atonde asanu, ana a nkhosa: asanu a caka
cimodzi; ndico copereka ca Nahesoni mwana wa Aminadabu.
18Tsiku laciwiri Netaneli mwana wa Zuwara, kalonga wa Isakara,
anabwera naco cace: 19anabwera naco copereka cace mbizi imodzi
yasiliva, kulemera kwace masekeli zana limodzi ndi makumi atatu,
mbale yowazira imodzi yasiliva ya masekeli makumi asanu ndi
awiri, kuyesa sekeli wa malo opatulika; zonse ziwiri zodzala ndi ufa

wosanganiza ndi mafuta, ukhale nsembe yaufa; 20cipande cimodzi
cagolidi ca masekeli khumi, codzala ndi cofukiza; 21ng'ombe
yamphongo imodzi, nkhosa yamphongo imodzi, mwana wa nkhosa
mmodzi wa caka cimodzi, zikhale nsembe yopsereza; 22tonde
mmodzi akhale nsembe yaucimo; 23ndi nsembe yoyamika,
ng'ombe ziwiri, nkhosa zamphongo zisanu, atonde asanu, ana a
nkhosa asanu a caka cimodzi; ndico copereka ca Netaneli mwana
wa Zuwara.
24Tsiku lacitatu kalonga wa ana a Zebuloni, ndiye Eliyabu mwana
wa Heloni: 25copereka cace ndico mbizi imodzi yasiliva, kulemera
kwace masekeli zana limodzi ndi makumi atatu, mbale yowazira
imodzi yasiliva ya masekeli makumi asanu ndi awiri, kuyesa sekeli
wa malo opatulika; zonse ziwiri zodzala ndi ufa wosanganiza ndi
mafuta, ukhale nsembe yaufa; 26cipande cimodzi cagolidi ca
masekeli khumi, codzala ndi cofukiza; 27ng'ombe yamphongo
imodzi, nkhosa yamphongo imodzi, mwana wa nkhosa mmodzi wa
caka cimodzi, zikhale nsembe yopsereza; 28tonde mmodzi akhale
nsembe yaucimo; 29ndi nsembe yoyamika, ng'ombe ziwiri, nkhosa
zamphongo zisanu, atonde asanu, ana a nkhosa asanu a caka
cimodzi; ndico copereka ca Eliyabu mwana wa Heloni.
30Tsiku lacinai Elizuri, mwana wa Sedeuri, kalonga wa ana a
Rubeni: 31copereka cace ndico mbizi imodzi yasiliva, kulemera
kwace masekeli zana limodzi ndi makumi atatu, mbale yowazira
imodzi yasiliva ya masekeli makumi asanu ndi awiri, kuyesa sekeli
wa malo opatulika, zonse ziwiri zodzala ndi ufa wosanganiza ndi
mafuta, ukhale nsembe yaufa; 32cipande cimodzi cagolidi ca
masekeli khumi, codzala ndi cofukiza; 33ng'ombe yamphongo
Imodzi, nkhosa yamphongo imodzi, mwana wa nkhosa mmodzi wa
caka cimodzi, zikhale nsembe yopsereza; 34tonde mmodzi akhale
nsembe yaucimo; 35ndi nsembe yoyamika, ng'ombe ziwiri, nkhosa
zamphongo zisanu, atonde asanu, ana a nkhosa asanu a caka
cimodzi; ndico copereka ca Elizuri mwana wa Sedeuri.
36Tsiku lacisanu kalonga wa ana a Simeoni, ndiye Selumiyeli,
mwana wa Zurisadai: 37copereka cace ndico mbizi imodzi yasiliva,
kulemera kwace masekeli zana limodzi ndi makumi atatu, mbale
yowazira imodzi yasiliva ya masekeli makumi asanu ndi awiri,
kuyesa sekeli wa malo opatulika; zonse ziwiri zodzala ndi ufa
wosanganiza ndi mafuta, ukhale nsembe yaufa; 38cipande cimodzi
cagolidi ca masekeli khumi, codzala ndi cofukiza; 39ng'ombe
yamphongo imodzi, nkhosa yamphongo imodzi, mwana wa nkhosa
mmodzi wa caka cimodzi, zikhale nsembe yopsereza; 40tonde
mmodzi akhale nsembe yaucimo; 41ndi nsembe yoyamika,
ng'ombe ziwiri, nkhosa zamphongo zisanu, atonde asanu, ana a

nkhosa asanu a caka cimodzi; ndico copereka ca Selumiyeli
mwana wa Zurisadai.
42Tsiku lacisanu ndi cimodzi, kalonga wa ana a Gadi, Eliyasafe
mwana wa Deyueli: 43copereka cace ndico mbizi imodzi yasiliva,
kulemera kwace masekeli zana limodzi ndi makumi atatu; mbale
yowazira Imodzi yasiliva ya masekeli makumi asanu ndi awiri,
kuyesa sekeli wa malo opatulika; zonse ziwiri zodzala ndi ufa
wosanganiza ndi mafuta, ukhale nsembe yaufa; 44cipande cimodzi
cagolidi ca masekeli khumi, codzala ndi cofukiza; 45ng'ombe
yamphongo imodzi, nkhosa yamphongo imodzi, mwana wa nkhosa
mmodzi wa caka cimodzi, zikhale nsembe yopsereza; 46tonde
mmodzi akhale nsembe yaucimo; 47ndi nsembe yoyamika,
ng'ombe ziwiri, nkhosa zamphongo zisanu, atonde asanu, ana a
nkhosa asanu a caka cimodzi; ndico copereka ca Eliyasafe mwana
wa Deyueli.
48Tsiku lacisanu ndi ciwiri kalonga wa ana a Efraimu Elisama
mwana wa Amihudi: 49copereka cace mbizi Imodzi yasiliva,
kulemera kwace masekeli zana limodzi ndi makumi atatu, mbale
yowazira imodzi ya masekeli makumi asanu ndi awiri, kuyesa
sekeli wa malo opatulika; zonse ziwiri zodzala ndi ufa wosanganiza
ndi mafuta, ukhale nsembe yaufa; 50cipande cimodzi cagolidi ca
masekeli khumi, codzala ndi cofukiza; 51ng'ombe yamphongo
imodzi, nkhosa yamphongo imodzi, mwana wa nkhosa mmodzi wa
caka cimodzi, zikhale nsembe yopsereza; 52tonde mmodzi akhale
nsembe yaucimo; 53ndi nsembe yoyamika, ng'ombe ziwiri, nkhosa
za mphongo zisanu, atonde asanu, ana a nkhosa asanu a caka
cimodzi; ndico copereka ca Elisama mwana wa Amihudi.
54Tsiku lacisanu ndi citatu kalonga wa ana a Manase ndiye
Gamaliyeli mwana wa Pedazuri: 55copereka cace ndico mbizi
imodzi yasiliva, kulemera kwace masekeli zana limodzi ndi makumi
atatu, mbale yowazira imodzi yasiliva ya masekeli makumi asanu
ndi awiri, kuyesa sekeli wa malo opatulika; zonse ziwiri zodzala ndi
ufa wosanganiza ndi mafuta, ukhale nsembe yaufa; 56cipande
cimodzi cagolidi ca masekeli khumi, codzala ndi
cofukiza; 57ng'ombe yamphongo imodzi, nkhosa yamphongo
imodzi, mwana wa nkhosa mmodzi wa caka cimodzi, zikhale
nsembe yopsereza; 58tonde mmodzi akhale nsembe
yaucimo; 59ndi nsembe yoyamika, ng'ombe ziwiri, nkhosa
zamphongo zisanu, atonde asanu, ana a nkhosa asanu a caka
cimodzi; ndico copereka ca Gamaliyeli mwana wa Pedazuri.
60Tsiku lacisanu ndi cinai kalonga wa ana a Benjamini, ndiye
Abidana mwana wa Gideoni: 61copereka cace ndico mbizi imodzi
yasiliva, kulemera kwace masekeli zana limodzi ndi makumi atatu,
mbale yowazira imodzi ya masekeli makumi asanu ndi awiri,

kuyesa sekeli wa malo opatulika; zonse ziwiri zodzala ndi ufa wosanganiza ndi mafuta, ukhale nsembe yaufa; 62cipande cimodzi cagolidi ca masekeli khumi, codzala ndi cofukiza; 63ng'ombe yamphongo imodzi, nkhosa yamphongo imodzi, mwana wa nkhosa mmodzi wa caka cimodzi, zikhale nsembe yopsereza; 64tonde mmodzi akhale nsembe yaucimo; 65ndi nsembe yoyamika, ng'ombe ziwiri, nkhosa zamphongo zisanu, atonde asanu, ana a nkhosa asanu a caka cimodzi; ndico copereka ca Abidana mwana wa Gideoni.
66Tsiku lakhumi kalonga wa ana a Dani, ndiye Ahiyezeri mwana wa Amisadai: 67copereka cace ndico mbizi imodzi yasiliva, kulemera kwace masekeli zana limodzi ndi makumi atatu, mbale yowazira imodzi yasiliva ya masekeli makumi asanu ndi awiri, kuyesa sekeli wa malo opatulika; zonse ziwiri zodzala ndi ufa wosanganiza ndi mafuta ukhale nsembe yaufa; 68cipande cimodzi cagolidi ca masekeli khumi, codzala ndi cofukiza; 69ng'ombe yamphongo imodzi, nkhosa yamphongo imodzi, mwana wa nkhosa mmodzi wa caka cimodzi, zikhale nsembe yopsereza; 70tonde mmodzi akhale nsembe yaucimo; 71ndi nsembe yoyamika, ng'ombe ziwiri, nkhosa zamphongo zisanu, atonde asanu, ana a nkhosa asanu a caka cimodzi; ndico copereka ca Ahiyezeri mwana wa Amisadai.
72Tsiku la khumi ndi limodzi kalonga wa ana a Aseri, ndiye Pagiyeli mwana wa Okirani; 73copereka cace ndico mbizi imodzi yasiliva, kulemera kwace masekeli zana limodzi ndi makumi atatu, mbale yowazira imodzi yasiliva ya masekeli makumi asanu ndi awiri, kuyesa sekeli wa malo opatulika; zonse ziwiri zodzala ndi ufa wosanganiza ndi mafuta, ukhale nsembe yaufa; 74cipande cimodzi cagolidi ca masekeli khumi, codzala ndi cofukiza; 75ng'ombe yamphongo imodzi, nkhosa yamphongo imodzi, mwana wa nkhosa mmodzi wa caka cimodzi, zikhale nsembe yopsereza; 76tonde mmodzi akhale nsembe yaucimo; 77ndi nsembe yoyamika, ng'ombe ziwiri, nkhosa zamphongo zisanu, atonde asanu, ana a nkhosa asanu a caka cimodzi; ndico copereka ca Pagiyeli mwana wa Okirani.
78Tsiku lakhumi ndi ciwiri kalonga wa ana a Nafitali, ndiye Ahira mwana wa Enani: 79copereka cace ndico mbizi imodzi yasiliva, kulemera kwace masekeli zana limodzi ndi makumi atatu, mbale yowazira imodzi yasiliva ya masekeli makumi asanu ndi awiri, kuyesa sekeli wa malo opatulika; zonse ziwiri zodzala ndi ufa wosanganiza ndi mafuta, ukhale nsembe yaufa; 80cipande cimodzi cagolidi ca masekeli khumi, codzala ndi cofukiza; 81ng'ombe yamphongo imodzi, nkhosa yamphongo imodzi, mwana wa nkhosa mmodzi wa caka cimodzi, zikhale nsembe yopsereza; 82tonde mmodzi akhale nsembe yaucimo; 83ndi nsembe yoyamika,

ng'ombe ziwiri, nkhosa zamphongo zisanu, atonde asanu, ana a nkhosa asanu a caka cimodzi; ici ndi copereka ca Ahira mwana wa Enani.
84Uku ndi kupereka ciperekere guwa la nsembe, ndi akalonga a Israyeli, tsiku la kudzoza kwace: mbizi zasiliva khumi ndi ziwiri, mbale zowazira zasiliva khumi ndi ziwiri, zipande zagolidi khumi ndi ziwiri; 85mbizi yasiliva yonse masekeli zana limodzi ndi makumi atatu, ndi mbale yowazira yonse masekeli makumi asanu ndi awiri; siliva wonse wa zotengerazo ndizo masekeli zikwi ziwiri ndi mazana anai, kuyesa sekeli wa malo opatulika. 86Zipande zagolidi ndizo khumi ndi ziwiri, zodzala ndi cofukiza, cipande conse masekeli khumi, kuyesa sekeli wa malo opatulika; golidi wonse wa zipandezo ndiwo masekeli zana limodzi ndi makumi awiri; 87ng'ombe zonse za nsembe yopsereza ndizo ng'ombe khumi ndi ziwiri, nkhosa zamphongo khumi ndi ziwiri, ana a nkhosa a caka cimodzi khumi ndi awiri, pamodzi ndi nsembe yao yaufa; ndi atonde a nsembe zaucimo khumi ndi awiri; 88ndi ng'ombe zonse za nsembe yoyamika ndizo ng'ombe makumi awiri ndi zinai, nkhosa zamphongo makumi asanu ndi limodzi, atonde makumi asanu ndi limodzi, ana a nkhosa a caka cimodzi makumi asanu ndi limodzi. Uku ndi kupereka ciperekere, litadzozedwa guwa la nsembe. 89Ndipo polowa Mose ku cihema cokomanako, kunena ndi iye, anamva Mau akunena naye ocokera ku cotetezerapo ciri pa likasa la mboni, ocokera pakati pa akerubi awiriwo; ndipo iye ananena naye.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Za kuyatsa nyalizo

1Ndipo Yehova ananena ndi Mose, nati, 2Nena kwa Aroni, nuti naye, Pamene uyatsa nyalizo, nyali manu ndi ziwirizo ziwale pandunji pace pa coikapo nyalico. 3Ndipo Aroni anacita cotero; anayatsa nyalizo kuti ziwale pandunji pace pa coikapo nyali, monga Yehova adauza Mose. 4Ndipo mapangidwe ace a coikapo nyali ndiwo golidi wosula; kuyambira tsinde lace kufikira maluwa ace anacisula; monga mwa maonekedwe ace Yehova anaonetsa Mose, momwemo anacipanga coikapo nyali.

Za kuyeretsa Alevi

5Ndipo Yehova ananena ndi Mose, nati, 6Uwatenge Alevi pakati pa ana a Israyeli, nuwayeretse. 7Ndipo utere nao kuwayeretsa: uwawaze madzi akucotsa zoipa, ndipo apititse lumo pa thupi lao lonse, natsuke zobvala zao, nadziyeretse. 8Pamenepo atenge ng'ombe yamphongo ndi nsembe yace yaufa, ufa wosanganiza ndi mafuta; utengenso ng'ombe yamphongo yina ikhale nsembe yaucimo. 9Ndipo ubwere nao Alevi pakhomo pa cihema cokomanako; nuwasonkhanitse khamu lonse la ana a Israyeli; 10nubwere nao Alevi pamaso pa Yehova; ndi ana a Israyeli aike manja ao pa Alevi; 11ndi Aroni apereke Alevi ngati nsembe yoweyula pamaso pa Yehova, yocokera kwa ana a Israyeli, kuti akhale akucita nchito ya Yehova, 12Ndipo Alevi aike manja ao pa mitu ya ng'ombezo; pamenepo ukonze imodzi ikhale nsembe yaucimo, ndi inzace, nsembe yopsereza za Yehova, kucita cotetezera Alevi. 13Ndipo uimike Alevi pamaso pa Aroni, ndi pamaso pa ana ace, ndi kuwapereka ngati nsembe yoweyula kwa Yehova. 14Momwemo upatule Alevi mwa ana a Israyeli; kuti Alevi akhale anga. 15Ndipo atatero alowe Alevi kucita Debito ya cihema cokomanako; ndipo uwayeretse, ndi kuwapereka ngati nsembe yoweyula. 16Pakuti aperekedwa konse kwa Ine ocokera mwa ana a Israyeli; ndadzitengera iwo m'malo mwa onse akutsegula m'mimba, ndiwo oyamba kubadwa a ana a Israyeli. 17Pakuti a oyamba kubadwa onse mwa ana a Israyeli ndi anga, mwa anthu ndi zoweta; tsiku lija ndinakantha oyamba kubadwa onse m'dziko la Aigupto, ndinadzipatulira iwo akhale anga. 18Ndipo ndatenga Alevi m'malo mwa oyamba kubadwa onse mwa ana a Israyeli. 19Ndipo ndapereka Alevi akhale mphatso ya kwa Aroni ndi ana ace amuna yocokera mwa ana a Israyeli, kucita nchito ya ana a Israyeli, m'cihema cokomanako ndi kucita cotetezera ana a Israyeli; kuti pasakhale mliri pakati pa ana a Israyeli, pakuyandikiza ana a Israyeli ku malo opatulika. 20Ndipo Mose ndi Aroni ndi khamu lonse la ana a Israyeli anacitira Alevi monga mwa zonse Yehova adauza Mose kunena za Alevi; momwemo ana a Israyeli

anawacitira. 21Ndipo Alevi anadziyeretsa, natsuka zobvala zao; ndi
Aroni anawapereka ngati nsembe yoweyula pamaso pa Yehova; ndi
Aroni anawacitira cotetezera kuwayeretsa. 22Ndipo atatero, Alevi
analowa kucita Debito yao m'cihema cokomanako pamaso pa
Aroni, ndi pamaso pa ana ace amuna; monga Yehova anauza Mose
kunena za Alevi, momwemo anawacitira.
23Ndipo Yehova ananena ndi Mose, nati, 24Ici ndi ca Alevi:
kuyambira ali wa zaka makumi awiri ndi zisanu ndi mphambu
azilowa kutumikira utumikiwu mu nchito ya cihema
cokomanako; 25ndipo kuyambira zaka makumi asanu azileka
kutumikira utumikiwu, osacitanso nchitoyi; 26koma atumikire
pamodzi ndi abale ao m'cihema cokomanako, kusunga udikirowo,
koma osagwira nchito. Utere nao Alevi kunena za udikiro wao.

Acita Paskha

1Ndipo Yehova ananena ndi Mose m'cipululu ca Sinai, mwezi
woyamba wa caka caciwiri ataturuka m'dziko la Aigupto, ndi
kuti, 2Ana a Israyeli acite Paskha pa nyengo yoikidwa. 3Tsiku
lakhumi ndi cinai la mweziwo, madzulo, muziucita, pa nyengo yace
yoikidwa; muucite monga mwa malemba ace onse, ndi maweruzo
ace onse. 4Ndipo Mose ananena ndi ana a Israyeli, kuti acite
Paskha. 5Ndipo anacita Paskha mwezi woyamba, tsiku lakhumi ndi
cinai la mweziwo, madzulo, m'cipululu ca Sinai; monga mwa zonse
Yehova adauza Mose, momwemo ana a Israyeli
anacita. 6Pamenepo panali amuna, anadetsedwa ndi mtembo wa
munthu, ndipo sanakhoza kucita Paskha tsiku lomwelo; m'mwemo
anafika pamaso pa Mose ndi pamaso pa Aroni tsiku
lomwelo; 7nanena naye amunawa, Tadetsedwa ife ndi mtembo wa
munthu; atiletseranji, kuti tisabwere naco copereka ca Yehova pa
nyengo yace yoikidwa, pakati pa ana a Israyeli? 8Ndipo Mose
ananena nao, Baimani; ndimve couza Yehova za inu.
9Ndipo Yehova ananena ndi Mose, nati, 10Nena ndi ana a Israyeli,
ndi kuti, Angakhale munthu wa inu kapena wa mibadwo yanu,
adetsedwa, cifukwa ca mtembo, kapena pokhala paulendo, koma
azicitira Yehova Paskha. 11Mwezi waciwiri, tsiku lace lakhumi ndi
cinai, madzulo, aucite; audye ndi mkate wopanda cotupitsa ndi
msuzi wowawa. 12Asasiyeko kufikira m'mawa, kapena kuthyolapo
pfupa; aucite monga mwa lemba lonse la Paskha. 13Munthu
akakhala woyera, wosakhala paulendo, koma akaleka kucita
Paskha, amsadze munthuyo kwa anthu a mtundu wace; popeza
sanabwera naco copereka ca Yehova pa nyengo yace yoikidwa,
munthuyu asenze kucimwa kwace. 14Ndipo mlendo akakhala mwa
inu, nakacitira Yehova Paskha, azicita monga mwa lemba la
Paskha, ndi monga mwa ciweruzo cace; lemba likhale limodzi kwa
inu, ndi kwa mlendo, ndi kwa wobadwa m'dziko.

Mtambo pamwamba pa kacisi

15Ndipo tsiku loutsa kacisi mtambo unaphimba kacisi, ndiwo
cihema cokomanako; ndipo madzulo padaoneka pakacisi ngati
moto, kufikira m'mawa. 16Kudatero kosalekeza; mtambo
umaciphimba, ndimoto umaoneka usiku, 17Ndipo pokwera mtambo
kucokera kucihema, utatero ana a Israyeli amayenda ulendo wao;
ndipo pamalo pokhala mtambo, pamenepo ana a Israyeli
amamanga mahema ao. 18Pakuwauza Yehova ana a Israyeli
amayenda ulendo, powauza Yehova amamanga mahema ao;
masiku onse mtambo ukakhala pamwamba pa kacisi amakhala
m'cigono. 19Ndipo pakukhalitsa mtambo masiku ambiri pamwamba
pa kacisi, pamenepo ana a Israyeli anasunga udikiro wa Yehova

osayenda ulendo. 20Ndipo pokhala mtambo pamwamba pa kacisi masiku pang'ono; pamenepo anakhala m'cigono monga awauza Yehova, nayendanso ulendo monga anauza Yehova. 21Koma mtambo ukakhala kuyambira madzulo kufikira m'mawa; pokwera mtambo m'mawa, ayenda ulendo; ngakhale msana ngakhale usiku, pokwera mtambo, ayenda ulendo. 22Ngakhale masiku awiri, kapena mwezi, kapena masiku ambiri, pokhalitsa mtambo pamwamba pa kacisi ndi kukhalapo, ana a Israyeli anakhala m'cigono, osayenda ulendo; koma pakukwera uwu, anayenda ulendo. 23Powauza Yehova amanga mahema, powauza Yehova ayenda ulendo; anasunga udikiro wa Yehova powauza Yehova mwa dzanja la Mose.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Adzipangira malipenga awiri asiliva

1Ndipo Yehova ananena ndi Mose, nati, 2Dzipangire malipenga awiri asiliva;
uwasule mapangidwe ace; ucite nao poitana khamu, ndi poyendetsa a
m'zigono. 3Akaliza, khamu lonse lisonkhane kuli iwe ku khomo la cihema
cokomanako, 4Akaliza limodzi, pamenepo akalonga, akuru a zikwi a m'Israyeli,
azisonkhana kuli iwe. 5Mukaliza cokweza, ayende a m'zigono za
kum'mawa. 6Mukalizanso cokweza, a m'zigono za kumwela ayende; alize
cokweza pakumuka. 7Pomemeza msonkhano mulize, wosati cokweza ai. 8Ana
amuna a Aroni, ansembe, ndiwo aziliza malipenga; ndipo akhale kwa inu
lemba losatha ku mibadwo yanu. 9Ndipo pamene mupita kunkhondo m'dziko
lanu kucita nkhondo pa mdani wakusautsa inu, mulize cokweza ndi
malipenga; ndipo Yehova Mulungu wanu adzakumbukila inu,
nadzakupulumutsani kwa adani anu. 10Momwemo tsiku lakukondwera inu, ndi
nyengo zoikidwa zanu, ndi poyamba miyezi yanu, muziliza malipenga pa
nsembe zanu zopsereza, ndi pa nsembe zanu zoyamika; ndipo akhale kwa inu
cikumbutso pamaso pa Mulungu wanu; Ine ndine Yehova Mulungu wanu.

Aisrayeli acoka ku Sinai

11Ndipo kunacitika, caka caciwiri, mwezi waciwiri, tsiku la makumi awiri la
mweziwo, kuti mtambo unakwera kucokera kwa kacisi wa mboni. 12Ndipo ana
a Israyeli anayenda monga mwa maulendo ao, kucokera m'cipululu ca Sinai;
ndi mtambo unakhala m'cipululu ca Parana. 13Potero anayamba ulendo wao
monga mwa mau a Yehova ndi dzanja la Mose. 14Ndipo anayamba kuyenda a
mbendera ya cigono ca ana a Yuda monga mwa magulu ao; woyang'anira
gulu lace ndiye Nahesoni mwana wa Aminadabu. 15Ndi pa gulu la pfuko la ana
a Isakara panali Netaneli mwana wa Zuwara. 16Ndi pa gulu la pfuko la ana a
Zebuloni panali Eliyabu mwana wa Heloni. 17Ndipo anagwetsa kacisi; ndi ana
a Gerisoni, ndi ana a Merari, akunyamula kacisi, anamuka naye. 18Ndi a
mbendera ya cigono ca Rubeni, anayenda monga mwa magulu ao; ndipo pa
gulu lace anayang'anira Elizuri mwana wa Sedeuri. 19Ndi pa gulu la pfuko la
ana a Simeoni anayang'anira Selumiyeli mwana wa Zurisadai. 20Ndi pa gulu la
pfuko la ana a Gadi anayang'anira Eliyasafe mwana wa Deyueli. 21Pamenepo
Akohati anayenda, ndi kunyamula zopatulika, ndi enawo anautsiratu kacisi
asanafike iwowa. 22Ndipo anayenda a mbendera ya cigono ca ana a Efraimu,
monga mwa magulu ao; ndi pa gulu lace anayang'anira Elizama mwana wa
Amihudi. 23Ndi pa gulu la pfuko la ana a Manase anayang'anira Gamaliyeli
mwana wa Pedazuri. 24Ndi pa gulu la pfuko la ana a Benjamini anayang'anira
Abidana mwana wa Gideoni. 25Pamenepo anayenda a mbendera ya cigono ca
ana a Dani, ndiwo a m'mbuyombuyo a zigono zonse, monga mwa magulu ao;
ndi pa gulu lace anayang'anira Ahiyezeri mwana wa Amisadai. 26Ndi pa gulu
la pfuko la ana a Aseri anayang'anira Pagiyeli mwana wa Okirani. 27Ndi pa
gulu la pfuko la ana a Nafitali anayang'anira Ahira mwana wa Enani. 28Potero
maulendo a ana a Israyeli anakhala monga mwa magulu ao; nayenda
ulendowao.

Mose apempha Hobabu awaperekeze

29Ndipo Mose anati kwa Hobabu mwana wa Reueli Mmidyani mpongozi wa
Mose, Ife tirikuyenda kumka ku malo amene Yehova anati, Ndidzakupatsani
awa; umuke nafe, tidzakucitira zokoma; popeza Yehova wanenera Israyeli
zokoma. 30Koma anati kwa iye, Sindidzamuka nanu; koma ndipita ku dziko
langa, ndi kwa abale anga. 31Koma anati, Usatisiyetu; popeza udziwa
poyenera kumanga ife m'cipululu, ndipo udzakhala maso athu. 32Ndipo

kudzatero, ukamuka nafe, inde, kudzali kuti zokoma ziri zonse Yehova aticitira ife, zomwezo tidzakucitira iwe.
33Ndipo anayenda kucokera ku phiri la Yehova ulendo wa masiku atatu; ndipo likasa la cipangano ca Yehova, linawatsogolera ulendo wa masiku atatu kuwafunira popumulira. 34Ndipo mtambo wa Yehova unali pamwamba pao msana, pakuyenda iwo kucokera kucigono. 35Ndipo kunali pakucoka kumka nalo likasa, Mose anati, Ukani Yehova, abalalike adani anu; akuda Inu athawe pamaso panu. 36Ndi pakupumula ili anati, Bwerani Yehova kwa zikwi zikwi za Israyeli.

Kudandaula kwa Aisrayeli

1Ndipo anthu anaipa, namadandaula m'makutu a Yehova; ndipo pamene
Yehova anamva anapsa mtima; ndi mota wa Yehova unayaka pakati pao,
nunyeketsa ku cilekezero ca cigono. 2Pamenepo anthu anapfuulira kwa Mose;
ndi Mose anapemphera kwa Yehova, ndi motowo unazimika. 3Ndipo anacha
malowo dzina lace Tabera; popeza moto wa Yehova udayaka pakati pao.
4Ndipo anthu osokonezeka ali pakati pao anagwidwa naco cilakolako; ndi ana
a Israyeli omwe analiranso, nati, Adzatipatsa nyama ndani? 5Tikumbukira
nsomba tinazidya m'Aigupto cabe, mankaka, ndi mavwendi, ndi anyesi a
mitundu itatu; 6koma tsopano moyo wathu waphwa; tiribe kanthu pamaso
pathu koma mana awa. 7Ndipo mana ananga zipatso zampasa, ndi
maonekedwe ace ngati maonekedwe a bedola. 8Anthu amamka, nawaola,
nawapera ndi mphero, kapena kuwasinja mumtondo, nawaphika m'mphika,
nawaumba timitanda; ndi powalawa anali ngati timitanda tokazinga ndi
mafuta. 9Ndipo pakugwa mame pacigono usiku, mana anagwapo.

Mose adandaulapa katundu wace

10Ndipo Mose anamva anthu alikulira m'mabanja ao, yense pakhomo pa
hema wace; ndipo Yehova anapsa mtima ndithu, ndipo kudamuipira
Mose. 11Ndipo Mose anati kwa Yehova, Munacitiranji coipa mtumiki wanu?
ndalekeranii kupeza ufulu pamaso panu, kuti muika pa ine katundu wa anthu
awa onse? 12Kodi ndinaima nao anthu awa onse? kodi ndinawabala, kuti
munene nane, Uwayangate ngati mlezi afukata khanda, kumka nao ku dzikolo
mudalumbirira makolo ao? 13Ndidzaiona kuti nyama yakuwapatsa anthu awa
onse? pakuti amalirira ine, ndi kuti, Tipatseni nyama, tidye. 14Sinditha
kuwasenza anthu awa onse ndekha, pakuti andilemera ine. 15Ndipo ngati
mundicitira cotero, mundiphetu tsopano apa, ngati ndapeza ufulu pamaso
panu, ndisayang'ane tsoka langa.
16Ndipo Yehova anati kwa Mose, Undisonkhanitsire amuna makumi asanu ndi
awiri mwa akuru a Israyeli, amene uwadziwa kuti ndiwo akuru a anthu, ndi
akapitao ao; nubwere nao ku cihema cokomanako, kuti aimeko pamodzi ndi
iwe. 17Pamenepo ndidzatsika ndi kulankhula nawe komweko; ndipo
ndidzatengako mzimu uti pa iwe, ndi kuika pa iwowa; adzakuthandiza kusenza
katundu wa anthu awa, kuti usasenze wekha. 18Ndipo unene ndi anthu,
Mudzipatuliretu, mawa mudzadya nyama; popeza mwalira m'makutu a
Yehova, ndi kuti, Adzatipatsa nyama ndani? popeza tinakhala bwino
m'Aigupto, Potero Yehova adzakupatsani nyama, ndipo
mudzadya. 19Simudzadya tsiku limodzi, kapena masiku awiri, kapena masiku
asanu, kapena masiku khumi, kapena masiku makumi awiri; 20koma mwezi
wamphumphu, kufikira ibwera m'mphuno mwako, ndi kuti ufukidwa nayo,
pakuti mwakaniza Yehova wakukhala pakati pa inu, ndi kulira pamaso pace,
ndi kuti, Tinaturukiranji m'Aigupto? 21Ndipo Mose anati, Anthu amene ndiri
pakati pao, ndiwo zikwi mazana asanu ndi limodzi oyenda pansi, ndipo Inu
mwanena, Ndidzawapatsa nyama, kuti adye mwezi wamphumphu. 22Kodi
adzawaphera magulu a nkhosa ndi ng'ombe, kuwakwanira? kapena kodi
nsomba zonse za m'nyanja zidzawasonkhanira pamodzi, kuwakwanira?
23Ndipo Yehova anati kwa Mose, Kodi dzanja la Mulungu lafupikira? tsopano
udzapenya ngati mau anga adzakucitikira kapena iai. 24Ndipo Mose
anaturuka, nauza anthu mau a Yehova; nasonkhanitsa akuru a anthu makumi
asanu ndi awiri, nawaimika pozungulira pa cihema. 25Ndipo Yehova anatsika
mumtambo, nanena nave, natengako mzimu uli pa iye, nauika pa akuru
makumi asanu ndi awiri; ndipo kunali kuti pokhala mzimu pa iwowa,

ananenera; koma osabwerezanso. 26Koma amuna awiri anatsalira m'cigono, dzina la wina ndiye Elidadi, dzina la mnzace ndiye Medadi; ndipo mzimuwo unakhala pa iwo; iwo ndiwo mwa oitanidwawo, koma sanaturuka kumka kucihema; ndipo ananenera m'cigono. 27Ndipo anathamanga anyamata, nauza Mose, nati, Elidadi ndi Medadi alikunenera m'cigono. 28Ndipo Yoswa mwana wa Nuni, mtumiki wa Mose kuyambira ubwana wace, anayankha nati, Mose, mfumu yanga, aletseni. 29Koma Mose anati kwa iye, Kodi ucita nsanje nao cifukwa ca ine? Mwenzi anthu onse a Yehova atakhala aneneri! mwenzi Yehova atawaikira mzimu wace! 30Ndipo Mose ndi akulu onse a Israyeli anasonkhana kucigono. 31Ndipo kudacokera mphepo kwa Yehova, nidza nazo zinziri zocokera kunyanja, nizitula kucigono, ulendo wa tsiku limodzi dera lino, ndi ulendo wa tsiku limodzi dera lina, pozungulira pa cigono, ndipo zinabisa nthaka ngati muyeso wa mikono iwiri. 32Ndipo anthu anauka tsiku lonselo, ndi usiku wace wonse, ndi mawa lace lonse, nakusa zinzirizo; wokusa pang'ono anakusa zodzaza mahomeri khumi; ndipo anadziyanikira izi pozungulira pa cigono. 33Nyamayi ikali pakati pa mano, asanaitafune, Mulungu anapsa mtima pa anthuwa, ndipo Yehova anawakantha anthu ndi kukantha kwakukuru ndithu. 34Ndipo anacha malowo dzina lace Kibiroti Hatava; popeza pamenepo anaika anthu osusuka. 35Kucokera ku Kibiroti Hatava anthuwo anayenda kumka ku Hazeroti; nakhala ku Hazeroti.

Numeri 12.

Miriamu ndi Aroni aukira Mose

1Ndipo Miriamu ndi Aroni anatsutsana naye Mose cifukwa ca mkazi mtundu
wace Mkusi amene adamtenga; popeza adatenga mkazi Mkusi. 2Ndipo anati,
Kodi Yehova wanena ndi Mose yekha? sananenanso ndi ife nanga? Ndipo
Yehova anamva. 3Koma munthuyu Mose ndiye wofatsa woposa anthu onse a
pa dziko lapansi. 4Ndipo Yehova anati kwa Mose, ndi Aroni, ndi Miriamu
modzidzimutsa, Turukani inu atatu kudza ku cihema cokomanako. Pamenepo
anaturuka atatuwo. 5Ndipo Yehova anatsika mumtambo njo, naima pa khomo
la cihema, naitana Aroni ndi Miriamu; naturuka onse awiri. 6Ndipo anati,
Tamvani tsono mau anga; pakakhala mneneri pakati pa inu, Ine Yehova
ndidzizindikiritsa kwa iye m'masomphenya, ndinena naye m'kulota. 7Satero
mtumiki wanga Mose; ndiye wokhulupirika m'nyumba mwanga
monse. 8Ndimanena naye pakamwa ndi pakamwa, maonekera, osati
mophiphiritsa; ndipo amapenyerera maonekedwe a Yehova; potero
munalekeranji kuopa kutsutsana naye mtumiki wanga, Mose. 9Pamenepo
Mulungu anawapsera mtima iwo; nawacokera iye. 10Ndipo mtambo unacoka
pacihema; ndipo taonani, Miriamu anali wakhate, wa mbu ngati cipale cofewa;
ndipo Aroni anapenya Miriamu, taonani, anali wakhate. 11Ndipo Aroni anati
kwa Mose, Mfumu yanga, musatiikiretu kucimwa kumene tapusa nako, ndi
kucimwa nako. 12Asakhaletu iye ngati wakufa, amene dera lina la mnofu wace
watha poturuka iye m'mimba mwa mace. 13Ndipo Mose anapfuulira kwa
Yehova, ndi kuti, Mciritsenitu, Mulungu, 14Ndipo Yehova anati kwa Mose, Atate
wace akadamlabvulira malobvu pankhope pace sakadacita manyazi masiku
asanu ndi awiri? ambindikiritse kunja kwa cigono masiku asanu ndi awiri;
ndipo atatero amlandirenso. 15Pamenepo anambindikiritsa Miriamu kunja kwa
cigono masiku asanu ndi awiri; ndipo anthu sanayenda ulendo kufikira
atamlandiranso Miriamu. 16Ndipo atatero anthuwo anamka ulendo wao
kucokera ku Hazeroti, namanga mahema ao m'cipululu ca Parana.

Atumidwa amuna 12 kukazonda Kanani

1Ndipo Yehova ananena ndi Mose, nati, 2Udzitumire amuna, kuti azonde dziko
la Kanani, limene ndirikupatsa ana a Israyeli; utumize munthu mmodzi wa
pfuko liri lonse la makolo ao, yense kalonga pakati pa anzace. 3Ndipo Mose
anawatumiza kucokera ku cipululu ca Parana monga mwa mau a Yehova;
amuna onsewa ndiwo akuru a ana a Israyeli. 4Maina ao ndi awa: wa pfuko la
Rubeni, Samuwa mwana wa Zakuri. 5Wa pfuko la Simeoni, Safati mwana wa
Hori. 6Wa pfuko la Yuda, Kalebi mwana wa Yefune. 7Wa pfuko la Isakara, Igali
mwana wa Yosefe. 8Wa pfuko la Efraimu, Hoseya mwana wa Nuni. 9Wa pfuko
la Benjamini, Paliti mwana wa Rafu. 10Wa pfuko la Zebuloni, Gadiyeli mwana
wa Sodi. 11Wa pfuko la Yosefe, wa pfuko la Manase, Gadi mwana wa
Susi. 12Wa pfuko la Dani, Amiyeli mwana wa Gemali. 13Wa pfuko la Aseri,
Setri mwana wa Mikayeli. 14Wa pfuko la Nafitali, Nabi mwana wa Vopisi. 15Wa
pfuko la Gadi, Geyuelimwana wa Maki. 16Awandi maina a amunawo Mose
anawatumira azonde dziko. Ndipo Mose anamucha Hoseya mwana wa Nuni
Yoswa. 17Potero Mose anawatuma azonde dziko la Kanani, nanena nao,
Kwerani uko kumwela, nimukwere kumapiri; 18mukaone dziko umo liriri; ndi
anthu akukhala m'mwemo, ngati ali amphamvu kapena ofok a, ngati acepa
kapena acuruka; 19ndi umo liriri dzikoli lokhalamo iwo, ngati lokoma, kapena
loipa; ndi umo iriri midziyo akhalamo iwo, ngati akhala poyera kapena
m'malinga; 20ndi umo iriri nthaka, ngati yopatsa, kapena yosuka, ngati pali
mitengo, kapena palibe, Ndipo limbikani mtima, nimubwere nazo zipatso za
m'dzikomo. Koma nyengoyi ndiyo nyengo yoyamba kupsa
mphesa. 21Pamenepo anakwerako, nazonda dziko kuyambira cipululu ca Zini
kufikira Rehobo, polowa ku Hamati. 22Ndipo anakwera njira ya kumwela nafika
ku Hebroni; ndi apa panali Ahimani, Sesai, ndi Talmai, ana a Anaki. (Koma
atamanga Hebroni zaka zisanu ndi ziwiri ndipo anamanga Zoani
m'Aigupto.) 23Ndipo anadza ku cigwa ca Esikolo, nacekako tsango limodzi la
mphesa, nalisenza awiri mopika; anabwera nazonso makangaza ndi
nkhuyu. 24Malowa anawacha cigwa ca Esikolo, cifukwa ca tsangolo ana a
Israyeli analicekako. 25Pamenepo anabwerera atazonda dziko, atatha masiku
makumi anai. 26Ndipo anamuka, nadza kwa Mose, ndi Aroni, ndi khamu lonse
la ana a Israyeli, ku cipululu ca Parana ku Kadesi; ndipo anabwezera mau
iwowa, ndi khamu lonse, nawaonetsa zipatso za dzikoli. 27Ndipo
anafotokozera, nati, Tinakafika ku dziko limene munatitumirako, ndilo ndithu a
moyenda mkaka ndi uci ngati madzi; ndi zipatso zace siizi. 28Komatu anthu
okhala m'dzikomo ngamphamvu; ndi midziyo nja malinga, yaikuru ndithu:
ndipo tinaonakonso ana a Anaki. 29Aamaleke akhala m'dziko la kumwera; ndi
Ahiti, ndi Ayebusi, ndi Aamori, akhala ku mapiri, ndi Akanani akhala kunyanja,
ndi m'mphepete mwa Yordano. 30Koma Kalebi anatontholetsa anthu pamaso
pa Mose, nati, Tikwere ndithu ndi kulilandira lathu lathu; popeza tikhozadi
kucita kumene. 31Koma anthu adakwera nayewo anati, Sitikhoza
kuwakwerera anthuwo; popeza atiposa mphamvu, 32Ndipo anaipsira ana a
Israyeli mbiri ya dziko adalizonda, nati, Dzikoli tapitamo kulizonda, ndilo dziko
lakutheramo anthu okhalamo; ndi anthu onse tidaona pakati pace ndiwo
anthu atali misinkhu. 33Tinaonakonso Anefili, ana a Anaki, obadwa ndi Anefili;
ndipo tinaoneka m'maso mwathu ngati zinsidzi; momwemonso tinaoneka
m'maso mwao.

Aisrayeli afuna kubwerera kumka ku Aigupto

1Pamenepo khamu lonse linakweza mau ao, napfuula; ndipo anthuwo analira
usikuwo. 2Ndipo ana onse a Israyeli anadandaulira Mose ndi Aroni; ndi khamu
lonse linanena nao, Mwenzi tikadafa m'dziko la Aigupto; kapena mwenzi
tikadafa m'cipululu muno! 3Ndipo Yehova atitengeranii kudza nafe kudziko
kuno, kuti tigwe nalo lupanga? Akazi athu ndi makanda athu adzakhala
cakudya cao; kodi sikuli bwino tibwerere ku Aigupto? 4Ndipo anati wina ndi
mnzace, Tiike mtsogoleri, tibwerere ku Aigupto. 5Pamenepo Mose ndi Aroni
anagwa nkhope pansi pamaso pa msonkhano wonse wa khamu la ana a
Israyeli. 6Ndipo Yoswa mwana wa Nuni, ndi Kalebi mwana wa Yefune, ndiwo a
iwo aja adazonda dzikolo, anang'amba zobvala zao; 7nanena ndi khamu lonse
la ana a Israyeli, nati, Dziko tapitamo kulizonda, ndilo dziko lokometsetsa
ndithu. 8Yehova akakondwera nafe, adzatilowetsa m'dzikomo, ndi kutipatsa
ilo; ndilo dziko moyenda mkaka ndi uci ngati madzi. 9Cokhaci
musamapikisana naye Yehova, musamaopa anthu a m'dzikomo; pakuti ndiwo
mkate wathu; mthunzi wao wawacokera, ndipo Yehova ali nafe;
musamawaopa. 10Koma khamu lonse lidati liwaponye miyala, Ndipo
ulemerero wa Yehova unaoneka m'cihema cokomanako kwa ana onse a
Israyeli.

Mose atetezera anthu kwa Mulungu

11Ndipo Yehova anati kwa Mose, Anthu awa adzaleka liti kundinyoza? ndipo
adzayamba liti kundikhulupirira, cinkana zizindikilo zonse ndinazicita pakati
pao? 12Ndidzawakantha ndi mliri, ndi kuwacotsera colowa cao, ndipo
ndidzakusandutsa iwe mtundu wa anthu waukuru ndi wamphamvu koposa
iwowa. 13Ndipo Mose anati kwa Yehova, Pamenepo Aaigupto adzamva;
popeza munakweza anthu awa ndi mphamvu yanu kuwacotsa pakati
pao; 14ndipo adzawauza okhala m'dziko muno; adamva kuti inu Yehova muli
pakati pa anthu awa; pakuti muoneka mopenyana, Yehova, ndi mtambo wanu
umaima pamwamba pao, ndipo muwatsogolera, ndi mtambo njo msana, ndi
moto njo usiku. 15Ndipo mukapha anthu awa ngati munthu mmodzi,
pamenepo amitundu amene adamva mbiri yanu adzanena, ndi kuti, 16Popeza
Yehova sanakhoza kuwalowetsa anthu awa m'dziko limene anawalumbirira,
cifukwa cace anawapha m'cipululu. 17Ndipo tsopano, ikuletu mphamvu ya
Mbuye wanga, monga mudanena, ndi kuti, 18Yehova ndiye wolekereza, ndi wa
cifundo cocuruka, wokhululukira mphulupulu ndi kulakwa, koma wosamasula
woparamula; wakuwalanga ana cifukwa ca mphulupulu ya atate ao, kufikira
mbadwo wacitatu ndi wacinai. 19Khululukiranitu mphulupulu ya anthu awa,
monga mwa cifundo canu cacikuru, ndi monga mudalekerera anthu awa,
kuyambira Aigupto kufikira tsopano. 20Ndipo Yehova anati, Ndakhululukira
monga mwa mau ako: 21koma ndithu, pali Ine, dziko lonse lapansi
lidzadzazidwa ndi ulemerero wa Yehova; 22popeza anthu onse awa amene
adaona ulemerero wanga, ndi zizindikilo zanga, ndidazicita m'Aigupto ndi
m'cipululu, koma anandiyesa Ine kakhumi aka, osamvera mau
anga; 23sadzaona dzikoli ndidalumbirira makolo ao, ngakhale mmodzi wa iwo
akundinyoza Ine, sadzaliona; 24koma mtumiki wanga Kalebi, popeza anali nao
mzimu wina, nanditsata monsemo, ndidzamlowetsa iyeyu m'dziko muja
analowamo; ndi mbeu zace zidzakhala nalo. 25Koma Aamaleki ndi Akanani
akhala m'cigwamo; tembenukani mawa, nimumke ulendo wanu kucipululu,
njira ya ku Nyanja Yofiira.

Odandaulawo saloledwa kulowa dziko la Kanani

26Ndipo Yehova ananena kwa Mose ndi Aroni, nati, 27Ndileke khamu loipa ili
lakudandaula pa Ine kufikira liti? Ndidamva madandaulo a ana a Israyeli,
amene amandidandaulira. 28Nunene nao, Pali Ine, ati Yehova, ndidzacitira inu
ndithu monga mwanena m'makutu mwanga; 29mitembo yanu idzagwa
m'cipululu muno; ndi owerengedwa anu onse, monga mwa kuwerenga kwanu
konse, kuyambira a zaka makumi awiri ndi mphambu, akudandaula pa
Ine; 30simudzalowa inu m'dzikolo, ndinakwezapo dzanja langa kukukhalitsani
m'mwemo, koma Kalebi mwana wa Yefune, ndi Yoswa mwana wa Nuni
ndiwo. 31Koma makanda anu, amene munanena za iwowa kuti adzakhala
cakudya, amenewo ndidzavalowetsa, ndipo adzadziwa dzikolo
mudalikana. 32Koma inu, mitembo yanu idzagwa m'cipululu muno. 33Ndipo
ana anu adzakhala oyendayenda m'cipululu zaka makumi anai, nadzasenza
kupulukira kwanu, kufikira mitembo yanu yatha m'cipululu. 34Monga mwa
kuwerenga kwa masiku amene munazonda dziko, masiku makumi anai, tsiku
limodzi kuwerenga caka cimodzi, mudzasenza mphulupulu zanu, zaka makumi
anai, ndipo mudzadziwa kuti ndaleka lonjezano langa. 35Ine Yehova ndanena,
ndidzacitira ndithu ici khamu ili lonse loipa lakusonkhana kutsutsana nane;
adzatha m'cipululu muno, nadzafamo. 36Ndipo amunawo, amene Mose
anawatumiza kukazonda dziko, amene anabwera nadandaulitsa khamu lonse
pa iye, poipsa mbiri ya dziko, 37amuna amene anaipsa mbiri ya dziko, anafa
ndi mliri pamaso pa Yehova. 38Koma Yoswa mwana wa Nuni, ndi Kalebi
mwana wa Yefune, anakhala ndi moyo mwa amuna aja adamukawo
kukazonda dziko. 39Ndipo Mose anauza ana a Israyeli mao onse awa; ndipo
anthu anamva cisoni cambiri. 40Ndipo anauka mamawa, nakwera pamwamba
pa, phiri, nati, Tiri pano, tidzakwera kumka ku malo amene Yehova ananena;
popeza tacimwa. 41Ndipo Mose anati, Mutero cifukwa ninji kulakwira mau a
Yehova, popeza simudzapindula nako? 42Musakwereko, pakuti Yehova sali
pakati pa inu; kuti angakukantheni adani anu. 43Pakuti Aamaleki ndi Akanani
ali komweko patsogolo panu, ndipo mudzagwa ndi lupanga; popeza
mwabwerera m'mbuyo osatsata Yehova, cifukwa cace Yehova sadzakhala
nanu. 44Koma anakwera pamwamba pa phiri modzikuza; koma likasa la
cipangano la Yehova, ndi Mose, sanacoka kucigono. 45Pamenepo anatsika
Aamaleki, ndi Akanani, akukhala m'phirimo nawakantha, nawapha kufikira ku
Horima.

Malamulo a pa nsembezo

1Ndipo Yehova ananena ndi Mose nati, 2Nena ndi ana a Israyeli,
nuti nao, Mukakalowa m'dziko lokakhalamo inu, limene
ndirikupatsa inu, 3ndipo mukakonzera Yehova nsembe yamoto,
nsembe yopsereza, kapena yophera, pocita cowinda ca padera,
kapena nsembe yaufulu, kapena nsembe ya pa nyengo zanu
zoikika, kumcitira Yehova pfungo lokoma, la ng'ombe kapena
nkhosa; 4pamenepo iye wobwera naco copereka cace kwa Yehova,
azibwera nayo nsembe yaufa, limodzi la magawo khumi la ufa
wosalala, wosanganiza ndi limodzi la magawo anai la bini la
mafuta; 5ndipo uzikonzera nsembe yopsereza kapena yophera,
vinyo wa nsembe yothira, limodzi la magawo anai la bini, ukhale
wa mwana wa nkhosa mmodzi. 6Kapena ukonzere nkhosa
yamphongo nsembe yaufa, awiri mwa magawo khumi a ufa
wosalala, wosanganiza ndi mafuta, limodzi la magawo atatu la
bini. 7Ndipo ubwere naye vinyo wa nsembe yothira, limodzi la
magawo atatu la bini, acitire Yehova pfungo lokoma. 8Ndipo
pamene mukonza ng'ombe ikhale nsembe yopsereza, kapena
yophera, kucita cowinda ca padera, kapena ikhale nsembe
yoyamika ya Yehova; 9abwere nayo, pamodzi ndi ng'ombeyo,
nsembe ya ufa wosalala, atatu mwa magawo khumi wosanganiza
ndi mafuta, limodzi la magawo awiri la bini. 10Ndipo ubwere naye
vinyo wa nsembe yothira limodzi la magawo awiri la hini, ndiye
nsembe yamoto ya pfungo: lokoma, ya Yehova. 11Kudzatero ndi
ng'ombe iri yonse, kapena nkhosa yamphongo iri yonse, kapena
mwana wa nkhosa ali yense, kapena mwana wa mbuzi ali
yense. 12Monga mwa kuwerenga kwace kwa izi muzikonza,
muzitero ndi yonse monga mwa kuwerenga kwace. 13Onse
akubadwa m'dzikomo acite izi momwemo, pobwera nayo kwa
Yehova nsembe yamoto ya pfungo lokoma. 14Ndipo akakhala nanu
mlendo, kapena ali yense wakukhala pakati pa inu mwa mibadwo
yanu, nakacitira Yehova nsembe yamoto ya pfungo lokoma; monga
mucita inu, momwemo iyenso, 15Kunena za khamu, pakhale lemba
limodzi kwa inu, ndi kwa mlendo wakukhala kwanu, ndilo lemba
losatha mwa mibadwo yanu; monga mukhala inu, momwemo
mlendo pamaso pa Yehova. 16Pakhale cilamulo cimodzi ndi
ciweruzo cimodzi kwa inu ndi kwa mlendo wakukhala kwanu.
17Ndipo Yehova ananena ndi Mose, nati, 18Nena ndi ana a Israyeli,
nuti nao, Pamene mulowa m'dziko limene
ndirikukulowetsani, 19kudzali, pakudya inu mkate wa m'dzikolo,
muzikwezera Yehova nsembe yokweza. 20Pa mtanda wanu
woyamba muperekeko kamtanda, kakhale nsembe yokweza;
monga mumacitira nsembe yokweza ya popuntha tirigu,

momwemo muzikakweza. 21Muzipatsa Yehova nsembe yokweza
yoitenga ku mtanda wanu woyamba, mwa mibadwo yanu.
22Ndipo pamene mulakwa, osacita mau awa onse amene Yehova
ananena ndi Mose; 23ndizo zonse Yehova anakuuzani ndi dzanja la
Mose, kuyambira tsikulo Yehova anauza, ndi kunkabe m'mibadwo
yanu; 24pamenepo kudzali, ngati anacicita osati dala, osacidziwa
khamulo, khamu lonse lipereke ng'ombe yamphongo ikhale
nsembe yopsereza, ya pfungo lokoma ya Yehova, pamodzi ndi
nsembe yace yaufa, ndi nsembe yace yothira, monga mwa
ciweruzo cace; ndi tonde mmodzi akhale nsembe yaucimo. 25Ndipo
wansembe azicita cotetezera khamu lonse la ana a Israyeli, ndipo
adzakhululukidwa; popeza sanacita dala, ndipo anadza naco
copereka cao, nsembe yamoto kwa Yehova, ndi nsembe yao
yaucimo pamaso pa Yehova, cifukwa ca kulakwa osati
dala. 26Ndipo khamu lonse la ana a Israyeli, adzakhululukidwa, ndi
mlendo yemwe wakukhala pakati pao; popeza khamu lonse
linacicita osati dala. 27Ndipo akacimwa munthu mmodzi osati dala,
abwere nayo mbuzi yamsoti ya caka cimodzi, ikhale nsembe
yaucimo. 28Ndipo wansembe acite comtetezera munthu
wakulakwa, osalakwa dala pamaso pa Yehova, kumcita
comtetezeraj ndipo adzakhululukidwa. 29Kunena za wobadwa
m'dziko mwa ana a Israyeli, ndi mlendo wakukhala pakati pao,
mukhale naco cilamulo cimodzi kwa iye wakucita kanthu kosati
dala. 30Koma munthu wakucita kanthu dala, ngakhale wobadwa
m'dziko kapena mlendo, yemweyo acitira Yehova mwano; ndipo
munthuyo amsadze pakati pa anthu a mtundu wace. 31Popeza
ananyoza mau a Yehova, nathyola lamulo lace; munthuyu amsadze
konse; mphulupulu yace ikhale pa iye.

Alangidwa wosasunsa Sabata

32Ndipo pokhala ana a Israyeli m'cipululu, anapeza munthu
wakufuna nkhuni tsiku la Sabata. 33Ndipo amene adampezawo
alinkufuna nkhuni anabwera naye kwa Mose ndi Aroni, ndi kwa
khamu lonse. 34Ndipo anathanga wamsunga, popeza
sicinanenedwa coyenera kumcitira iye. 35Ndipo Yehova anati kwa
Mose, Amuphe munthuyu ndithu; khamu lonse limponye miyala
kunja kwa cigono. 36Pamenepo khamu lonse linamturutsa kunja
kwa cigono, ndi kumponya miyala, ndipo anafa; monga Yehova
adauza Mose.

Pakhale cizindikilo pa zobvala zao

37Ndipo Yehova ananena ndi Mose, nati, 38Nena ndi ana a Israyeli,
nuwauze kuti adziombere mphonje m'mphepete mwa zobvala zao,
mwa mibadwo yao, naike pamphonje m'mphepetemo thonje
lamadzi. 39Ndipo cikhale kwa inu mphonje, yakuti
muziyang'anirako, ndi kukumbukila malamulo onse a Yehova, ndi

kuwacita, ndi kuti musamazondazonda kutsata za m'mtima
mwanu, ndi za m'maso mwanu zimene mumatsata ndi
cigololo; 40kuti mukumbukile ndi kucita malamulo anga onse, ndi
kukhala wopatulikira Mulungu wanu. 41Ine ndine Yehova Mulungu
wanu, wakukuturutsani m'dziko la Aigupto, kuti ndikhale Mulungu
wanu; Ine ndine Yehova Mulungu wanu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Kora, Datani, ndi Abiramu aukira Mose

1Koma Kora, mwana wa Izara, mwana wa Kohati, mwana wa Levi, anatenga
Datani ndi Abiramu, ana a Eliyabu, ndi Oni mwana wa Peleti, ana a
Rubeni; 2ndipo anauka pamaso pa Mose, pamodzi ndi amuna: mazana awiri
mphambu makumi asanu a ana a Israyeli, ndiwo akalonga a khamulo,
oitanidwa a msonkhano, amuna omveka. 3Ndipo anasonkhana motsutsana pa
Mose ndi Aroni, nanena nao, Mukula mphamvu inu, pakuti khamu lonse
nlopatulika, onsewa, ndipo Yehova ali pakati pao; mudzikuza bwanji pa
msonkhano wa Yehova? 4Pamene Mose anamva ici anagwa nkhope yace
pansi; 5nanena ndi Kora ndi khamu lace lonse, ndi kuti, M'mawa Yehova
adzatizindikiritsa anthu ace ndi ayani, wopatulika ndani, amene
adzamsendeza pafupi pa iye; ndi iye amene anamsankha adzamsendeza
pafupi pa iye. 6Citani ici; dzitengereni mbale za zofukiza, Kora, ndi khamu lace
lonse; 7nimuikemo moto, muikenso cofukiza pamenepo, pamaso pa Yehova,
mawa; ndipo kudzali kuti amene Yehova amsankha, wopatulika ndiye;
mwakula mphamvu, inu ana a Levi. 8Ndipo Mose ananena ndi Kora, Tamvani
tsono, inu ana a Levi; 9kodi muciyesa cinthu cacing'ono, kuti Mulungu wa
Israyeli anakusiyanitsani ku khamu la Israyeli, kukusendezani pafupi pa iye,
kucita nchito ya kacisi wa Yehova, ndi kuima pamaso pa khamu
kuwatumikira; 10ndi kuti anakusendeza iwe, ndi abale ako onse, ana a Levi,
pamodzi ndi iwe? ndipo kodi mufunanso nchito ya nsembe? 11Cifukwa cace,
iwe ndi khamu lonse mwasonkhana kutsutsana ndi Yehova; ndipo Aroniyo
ndani, kuti mudandaule pa iye? 12Ndipo Mose anatuma kukaitaniza Datani ndi
Abiramu, ana a Eliyabu; koma anati, Sitifikako: 13kodi ndi cinthu cacing'ono
kuti watikweza kuticotsa m'dziko moyenda mkaka ndi uci ngati madzi, kutipha
m'cipululu; koma udziyesanso ndithu kalonga wa ife? 14Ndiponso
sunatilowetsa m'dziko moyenda mkaka ndi uci ngati madzi, kapena kutipatsa
colowa ca minda, ndi minda yamphesa; kodi udzakolowola amuna awa maso
ao? Sitifikako. 15Pamenepo Mose adapsa mtima, ndipo anati kwa Yehova,
Musasamalira copereka cao; siodinalanda buru wao mmodzi, kapena kucitira
coipa mmodzi wa iwowa. 16Ndipo Mose anati kwa Kora, Iwe ndi khamu lako
lonse mukhale pamaso pa Yehova mawa, iwe ndi iwowa, ndi
Aroni; 17nimutenge munthu yense mbale yace yofukizamo, nimuike cofukiza
m'mwemo, nimubwere nazo, yense mbale yace yofukizamo pamaso pa
Yehova, mbale zofukizamo mazana awiri ndi makumi asanu; ndi iwe, ndi Aroni,
yense mbale yace yofukizamo. 18Potero munthu yense anatenga mbale yace
yofukizamo, naikamo moto, naikapo cofukiza, naima pa khomo la cihema
cokomanako pamodzi ndi Mose ndi Aroni. 19Ndipo Kora anasonkhanitsa
khamu lonse mopikisana nao ku khomo la cihema cokomanako; ndipo
ulemerero wa Yehova unaoneka kwa khamu lonse.

Alangidwa oukirawo

20Ndipo Yehova ananena ndi Mose ndi Aroni, nati, 21Dzipatu, leni pakati pa
khamu lino, kuti ndi wathe m'kamphindi. 22Ndipo anagwa nkhope zao pansi,
nati, Mulungu, ndinu Mulungu wa mizimu ya anthu onse, walakwa munthu
mmodzi, ndipo kodi mukwiya nalo khamu lonse? 23Ndipo Yehova ananena ndi
Mose, nati, 24Nena ndi khamulo, ndi kuti, Kwerani kucoka pozungulira
mahema a Kora, Datani, ndi Abiramu. 25Ndipo Mose anauka namuka kwa
Datani ndi Abiramu; ndi akuru a Israyeli anamtsata. 26Ndipo ananena ndi
khamulo, nati, Cokanitu ku mahema a anthu awa oipa, musamakhudza kanthu
kao kali konse, mungaonongeke m'zocimwa zao zonse. 27Potero anakwera
kucokera pozungulira mahema a Kora, Datani, ndi Abiramu, ndipo Datani ndi

Abiramu anaturuka, naima pakhomo pa mahema ao, ndi akazi ao, ndi ana ao amuna, ndi makanda ao. 28Ndipo Mose anati, Ndi ici mudzadziwa kuti Yehova wanditumiza ine kucita nchito izi zonse, ndi kuti sizifuma m'mtima mwanga mwanga. 29Akafa anthu awa monga amafa anthu onse, kapena akasungika monga amasungika anthu onse, Yehova sananditumiza ine. 30Koma Yehova akalenga cinthu catsopano, ndi nthaka ikayasama pakamwa pace, nikawameza ndi zonse ali nazo, nakatsikira iwo kumanda ali ndi moyo; pamenepo mudzadziwa kuti anthu awa anyoza Mulungu. 31Ndipo kunali, pakutha iye kunena mau awa onse, nthaka inang'ambika pansi pao; 32ndi dziko linayasama pakamwa pace ndi kuwameza, iwo ndi mabanja ao, ndi amuna ao onse akutsata Kora, ndi akatundu ao onse. 33Comweco iwowa, ndi onse anali nao, anatsikira kumanda ali ndi moyo, ndi dziko linasunama pa iwo, ndipo anaonongeka pakati pa msonkhano. 34Ndipo Aisrayeli onse akukhala pozinga pao anathawa pakumva kupfuula kwao; pakuti anati, Lingatimeze dziko ifenso. 35Ndipo mota unaturuka kwa Yehova, ndi kunyeketsa amuna mazana awiri ndi makumi asanu aja akubwera naco cofukiza.

Alanditsa mbale zofukiza za oukirawo

36Ndipo Yehova ananena ndi Mose, nati, 37Nena ndi Eleazara mwana wa Aroni wansembe, kuti aphule mbale zofukiza pakati pa moto, nutaye makalawo uko kutali; pakuti ziri zopatulika; 38mbale zofukizazo za iwo amene adacimwira moyo wao wao, ndipo azisule zaphanthiphanthi, zikhale cibvundikilo ca guwa la nsembe; popeza anabwera nazo pamaso pa Yehova, cifukwa cace zikhala zopatulika; ndipo zidzakhala cizindikilo kwa ana a Israyeli. 39Ndipo Eleazara wansembe anatenga mbale zofukiza zamkuwa, zimene anthu opsererawo adabwera nazo; ndipo anazisula zaphanthiphanthi zikhale cibvundikilo ca guwala nsembe; 40cikhale cikumbutso kwa ana a Israyeli, kuti mlendo, wosati wa mbeu ya Aroni, asasendere kucita cofukiza pamaso pa Yehova; angakhale monga Kora ndi khamu lace; monga Yehova adanena naye ndi dzanja la Mose.

Anthu adandaula, mliri uwaononga

41Koma m'mawa mwace khamu lonse la ana a Israyeli anadandaula pa Mose ndi Aroni, nati, Mwapha anthu a Yehova, inu. 42Ndipo kunali, posonkhanidwa khamulo kutsutsana nao Mose ndi Aroni, kuti anaceukira cihema cokomanako; taonani, mtambo unaciphimba, ndi ulemerero wa Yehova unaoneka. 43Ndipo Mose ndi Aroni anadza kukhomo kwa cihema cokomanako. 44Ndipo Yehova ananena ndi Mose, nati, 45Kwerani kucoka pakati pa khamu lino, kuti ndiwathe m'kamphindi. Pamenepo adagwa nkhope zao pansi. 46Ndipo Mose anati kwa Aroni, Tenga mbale yako yofukiza, nuikemo mota wa ku guwa la nsembe, nuikepo cofukiza, nufulumire kumuka ku khamulo, nuwacitire cowatetezera; pakuti waturuka mkwiyo pamaso pa Yehova; wayamba mliri. 47Ndipo Aroni anatenga monga Mose adanena, nathamanga kulowa pakati pa msonkhano; ndipo taonani, udayamba mliri pakati pa anthu; ndipo anaikapo cofukiza nawacitira anthu cowatetezera. 48Ndipo anaima pakati pa akufa ndi amoyo; ndi mliri unaleka. 49Koma akufa nao mliri ndiwo zikwi khumi ndi zinai mphambu mazana asanu ndi awiri, osawerenga aja adafera cija ca Kora. 50Ndipo Aroni anabwera kwa Mose ku khomo la cihema cokomanako; ndi mliri unaleka.

Ndodo ya Aroni iphuka

1Ndipo Yehova ananena ndi Mose, nati, 2Nena ndi ana a Israyeli, nulandire
kwa yense ndodo, banja liri onse la makolo ndodo imodzi, mafuko ao onse
monga mwa mabanja a makolo ao azipereka ndodo, zikhale khumi ndi ziwiri;
nulembe dzina la yense pa ndodo yace. 3Ndipo ulembe dzina la Aroni pa
ndodo ya Levi; pakuti pakhale ndodo imodzi pa mkuru yense wa nyumba za
makolo ao. 4Ndipo uziike m'cihema cokomanako, cakuno ca mboni, kumene
ndikomana ndi inu. 5Ndipo kudzali, kuti ndodo ya munthu ndimsankheyo,
idzaphuka; ndipo ndidzadziletsera madandaulo a ana a Israyeli amene
adandaula nao pa inu. 6Ndipo Mose ananena ndi ana a Israyeli, ndipo
akalonga ao onse anapereka, yense ndodo imodzi, monga mwa mabanja a
makolo ao, ndodo khumi ndi ziwiri; ndi ndodo ya Aroni inakhala pakati pa
ndodo zao. 7Ndipo Mose anaika ndodozo pamaso pa Yehova m'cihema ca
mboni. 8Ndipo kunali m'mawa mwace, kuti Mose analowa m'cihema ca mboni;
ndipo taonani, ndodo ya Aroni, ya pa banja la Levi, inaphuka, nionetsa
timaani, nicita maluwa, nipatsa akatungurume. 9Ndipo Mose anaturutsa
ndodo zonse kuzicotsa pamaso pa Yehova, azione ana onse a Israyeli; ndipo
anapenya, natenga yense ndodo yace. 10Ndipo Yehova anati kwa Mose,
Bweza ndodo ya Aroni kulika cakuno ca mboni, isungike ikhale cizindikilo ca
pa ana opikisana; kuti unelitsirizire madandaulo ao, kuti ungafe. 11Ndipo Mose
anacita monga Yehova adamuuza, momwemo anacita.
12Pamenepo ana a Israyeli ananena ndi Mose, nati, Taonani, tikufa,
tionongeka, tionongeka tonse. 13Yense wakuyandikiza kacisi wa Yehova
amwalira; kodi tidzatha nkufa?

Udindo wa ansembe ndi Alevi, ndi zolandira zao

1Ndipo Yehova anati kwa Aroni, Iwe ndi ana ako amuna ndi banja la kholo lako
pamodzi ndi iwe muzisenza mphulupulu ya malo opatulika; ndipo iwe ndi ana
ako amuna pamodzi ndi iwe musenze mphulupulu ya nchito yanu ya
nsembe. 2Ndiponso abale ako, pfuko la Alevi, pfuko la kholo lako,
uwayandikizitse pamodzi ndi iwe, kuti aphatikane ndi iwe, ndi kukutumikira;
koma iwe ndi ana ako pamodzi ndi iwe mukhale ku khomo la cihema ca
mboni. 3Ndipo asunge udikiro wako, ndi udikiro wa cihema conse; koma
asayandikize zipangizo za malo opatulika, ndi guwa la nsembe, kuti mungafe,
iwo ndi inu. 4Koma aziphatikana nawe, nazisunga udikiro wa cihema
cokomanako, kucita nchito yonse ya cihema; koma mlendo asayandikize
inu. 5Ndipo musunge udikiro wa malo opatulika, ndi udikiro wa guwa la
nsembe; kuti pasakhalenso mkwiyo pa ana a Israyeli. 6Ndipo Ine, taonani,
ndinatenga abale anu Alevi kuwacotsa pakati pa ana a Israyeli; ndiwo
mphatso yanu, yopatsidwa kwa Yehova, kucita nchito ya cihema
cokomanako. 7Ndipo iwe ndi ana ako amuna pamodzi ndi iwe mucite nchito
yanu ya nsembe, pa zonse za ku guwa la nsembe, ndi za m'kati mwa nsaru
yocinga; ndipo mutumikire; ndikupatsani nchito yanu ya nsembe, utumiki
wopatsika kwaulere; koma mlendo wakuyandikiza amuphe.
8Ndipo Yehova ananena ndi Aroni, Ndipo taona, Ine ndakupatsa udikiro wa
nsembe zanga zokweza, ndizo zopatulika zonse za ana a Israyeli; cifukwa ca
kudzozedwaku ndazipereka kwa iwe, ndi kwa ana ako amuna, likhale lemba
losatha. 9Izi ndi zako pa zinthu zopatulikitsa, zosafika kumoto; zopereka: zao
zonse, ndi nsembe zao zonse zaufa, ndi nsembe zao zonse zaucimo, ndi
nsembe zao zonse zoparamula, zimene Andibwezera Ine, zikhale zopatulikitsa
za iwe ndi za ana ako amuna. 10Muzizidya izi monga zopatulikitsa; mwamuna
yense adyeko; uziyese zopatulika. 11Zako ndi izinso: nsembe yokweza ya
mphatso yao, ndi nsembe zoweyula zonse za ana a Israyeli; ndazipereka kwa
iwe, ndi kwa ana ako amuna ndi kwa ana ako akazi pamodzi ndi iwe, likhale
lemba losatha; oyera onse a m'banja lako adyeko. 12Mafuta onse
okometsetsa, ndi vinyo watsopano, ndi tirigu yense wokometsetsa, zipatso
zao zoyamba zimene aziperekako kwa Yehova, ndazipereka kwa
iwe. 13Zipatso zoyamba zonse ziri m'dziko mwao, zimene amadza nazo kwa
Yehova, zikhale zako; oyera onse a m'banja lako adyeko. 14Ziri zonse
zoperekedwa ciperekere m'Israyeli ndi zako. 15Ziri zonse zoyambira kubadwa
mwa zamoyo zonse zimene abwera nazo kwa Yehova, mwa anthu ndi mwa
nyama, ndi zako; koma munthu woyamba kubadwa uzimuombola ndithu; ndi
nyama yodetsa yoyamba kubadwa uziiombola. 16Ndipo zimene ziti
zidzaomboledwa uziombole kuyambira za rowezi umodzi, monga mwa kuyesa
kwako, pa ndarama za masekeli asanu, kuyesa sekeli wa malo opatulika,
ndiwo magera makumi awiri. 17Koma ng'ombe yoyamba kubadwa, kapena
nkhosa yoyamba kubadwa, kapena mbuzi yoyamba kubadwa, usaziombola;
ndizo zopatulika; uwace mwazi wace pa guwa la nserobe, ndi kufukiza mafuta
ao, nsembe yamoto ya pfungo lokoma kwa Yehova. 18Ndipo nyama yace ndi
yako, ndiyo nganga ya nsembe yoweyula ndi mwendo wathako wa kulamanja,
ndizo zako. 19Nsembe zokweza zonse za zinthu zopatulika, zimene ana a
Israyeli azikweza kwa Yehova, ndazipereka kwa iwe, ndi kwa ana ako amuna
ndi kwa ana ako akazi pamodzi ndi iwe, likhale lemba losatha; ndilo pangano
lamcere losatha, pamaso pa Yehova, kwa iwe ndi mbeu zako pamodzi ndi
iwe. 20Ndipo Yehova ananena ndi Aroni, Ulibe colowa m'dziko lao, ulibe gawo
pakati pao; Ine ndine gawo lako ndi colowa cako pakati pa ana a Israyeli.

Limodzi la magawo khumi ndilo gawo la ansembe

21Ndipo taonani, ndawaninkha ana a Levi limodzi la magawo khumi mwa
zonse m'Israyeli, likhale colowa cao, mphotho ya pa nchito yao alikuicita,
nchito ya cihema cokomanako. 22Ndipo kuyambira tsopano ana a Israyeli
asayandikize cihema cokomanako, angamasenze ucimo kuti angafe. 23Koma
Alevi azicita nchito ya cihema cokomanako, iwo ndiwo azisenza mphulupulu
yao; ndilo lemba losatha mwa mibadwo yanu; ndipo asakhale naco colowa
pakati pa ana a Israyeli. 24Popeza ndapatsa Alevi limodzi la magawo khumi, la
ana a Israyeli, limene apereka nsembe, yokweza kwa Yehova, likhale colowa
cao; cifukwa cace ndanena nao, Asadzakhale naco colowa mwa ana a Israyeli.
25Ndipo Yehova ananena ndil Mose, nati, 26Unenenso ndi Alevi, nuti nao,
Pamene mulandira kwa ana a Israyeli, limodzi la magawo khumi limene
ndakupatsani likhale colowa canu cocokera kwao, muziperekako nsembe
yokweza ya Yehova, limodzi la magawo khumi la limodzi la magawo
khumi. 27Ndipo akuyesereninso nsembe yanu yokweza monga tirigu wa
padwale, monga mopondera mphesa modzala. 28Momweno inunso
muzipereka kwa Yehova nsembe yokweza yocokera ku magawo anu onse a
magawo khumi, a zonse muzilandira kwa ana a Israyeli; ndipo muperekeko
nsembe yokweza ya Yehova kwa Aroni wansembe. 29Mupereke nsembe
zokweza zonse za Yehova kuzitenga ku mphatso zanu zonse, kusankhako
zokometsetsa ndizo zopatulika zace. 30Cifukwa cace unene nao, Pamene
mukwezako zokometsetsa zace, zidzayesedwanso kwa Alevi ngati zipatso za
padwale, ndi zipatso za mopondera mphesa, 31Ndipo muzidye pamalo ponse,
inu ndi a pabanja panu; popeza ndizo mphotho yanu mwa nchito yanu
m'cihema cokomanako. 32Ndipo simudzasenzapo ucimo, mutakwezako
zokometsetsa zace; ndipo musamaipsa zinthu zopatulika za ana a Israyeli,
kuti mungafe.

Za ng'ombe yamsoti yofiira ndi madzi oyeretsa nao

1Ndipo Yehova ananena ndi Mose ndi Aroni, nati, 2Ili ndi lemba la cilamulo
Yehova adalamuliraci, ndi kuti, Nena ndi ana a Israyeli kuti azikutengera
ng'ombe ramsoti yofiira, yangwiro yopanda enema, yosamanga m'goli; 3ndipo
muipereke kwa Eleazara wansembe, naiturutse iye kunja kwa cigono, ndipo
wina aiphe pamaso pace. 4Ndipo Eleazara wansembe atengeko mwazi wace
ndi cala cace, nawazeko mwazi wace kasanu ndi kawiri pakhomo pa cihema
cokomanako. 5Pamenepo atenthe ng'ombe yamsotiyo pamaso pace; atenthe
cikopa cace ndi nyama yace, ndi mwazi wace, pamodzi ndi cipwidza
cace. 6Ndipo wansembe atenge mtengo wamkungudza, ndi hisope, ndi
ubweya wofiira, naziponye pakati pa mota irikupsererapo ng'ombe
yamsoti. 7Pamenepo wansembe atsuke zobvala zace, nasambe thupi lace ndi
madzi; ndipo atatero alowenso kucigono; koma wansembeyo adzakhala
wodetsedwa kufikira madzulo. 8Ndipo iye wakutentha ng'ombeyo atsuke
zobvala zace, nasambe thupi lace ndi madzi, nadzakhala wodetsedwa kufikira
madzulo. 9Ndipo munthu woyera aole mapulusa a ng'ombe ya msotiyo,
nawaike kunja kwa cigono, m'malo moyera: ndipo awasungire khamu la ana a
lsrayeli akhale a madzi akusiyanitsa; ndiwo nsembe yaucimo. 10Ndipo
wakuola mapulusayo a ng'ombe ya msoti atsuke zobvala zace, nadzakhala
wodetsedwa kufikira madzulo; ndipo likhale lemba losatha kwa ana a Israyeli,
ndi kwa mlendo wakukhala pakati pao. 11Iye wakukhudza mtembo wa munthu
ali yense adzakhala wodetsedwa masiku asanu ndi awiri; 12iyeyo adziyeretse
nao tsiku lacitatu, ndi pa tsiku lacisanu ndi ciwiri adzakhala woyera; koma
akapanda kudziyeretsa tsiku lacitatu, sadzakhala woyera tsiku lacisanu ndi
ciwiri. 13Ali yense wakukhudza mtembo wa munthu ali yense wakufa,
osadziyeretsa, aipsa kacisi wa Yehova; amsadze munthuyo kwa Israyeli;
popeza sanamwaza madzi akusiyanitsa; ndiye wodetsedwa; kudetsedwa
kwace kukali pa iye. 14Cilamulo ndi ici: Munthu akafa m'hema, yense
wakulowa m'hemamo, ndi yense wakukhala m'hemamo, adzakhala
wodetsedwa masiku asanu ndi awiri. 15Ndi zotengera zonse zobvundukuka,
zopanda cibvundikilo comangikapo, ziri zodetsedwa. 16Ndipo ali yense
wakukhudza munthu wophedwa ndi lupanga, kapena mtembo, kapena pfupa
la munthu, kapena manda, pathengo poyera, adzakhala wodetsedwa masiku
asanu ndi awiri. 17Ndipo atengereko wodetsedwayo mapulusa akupsererawo a
nsembe yaucimo, nathirepo m'cotengera madzi oyenda; 18ndi munthu woyera
atenge hisope, nambviike m'madzimo, ndi kuwawaza pahema ndi pa
zotengera zonse, ndi pa anthu anali pomwepo, ndi pa iye wakukhudza pfupa,
kapena wophedwa, kapena wakufa, kapena Manda. 19Ndipo woyerayo awaze
pa wodetsedwayo tsiku lacitatu, ndi tsiku lacisanu ndi ciwiri; ndipo tsiku
lacisanu ndi ciwiri amyeretse; ndipo atsuke zobvala zace, nasambe m'madzi,
nadzakhala woyera madzulo. 20Koma munthu wakukhala wodetsedwa, koma
wosadziyeretsa, azimsadza munthuyo pakati pa msonkhano, popeza waipsa
malo opatulika a Yehova; sanamwaza madzi akusiyanitsa; ndiye
wodetsedwa. 21Ndipo likhale kwa iwo lemba losatha; kuti iye wakuwaza madzi
akusiyanitsa azitsuka zobvala zace; ndi iye wakukhudza madzi akusiyanitsa
adzakhala wodetsedwa kufikira madzulo. 22Ndipo ciri conse munthu
wodetsedwa acikhudza cidzakhala codetsedwa; ndi munthu wakucikhudza
adzakhala wodetsedwa kufikira madzulo.

Imfa ya Miriamu; madzi a Meriba

1Ndipo ana a Israyeli, ndilo khamu lonse, analowa m'cipululu ca Zini mwezi
woyamba; ndipo anthu anakhala m'Kadesi; kumeneko anafa Miriamu,
naikidwakomweko. 2Ndipo khamulo linasowa madzi; pamenepo anasonkhana
kutsutsana nao Mose ndi Aroni. 3Ndipo anthu anatsutsana ndi Mose, nanena,
nati, Mwenzi titangomwalira muja abale athu anamwalira pamaso pa
Yehova! 4Mwalowa nao bwanji msonkhano wa Yehova m'cipululu muno, kuti
tifere mommuno, ife ndi zoweta zathu? 5Ndipo munatikwezeranji kutiturutsa
m'Aigupto, kutilowetsa m'malo oipa ano? Si malo a mbeu awa, kapena mkuyu,
kapena mpesa kapena makangaza; ngakhale madzi akumwa palibe. 6Ndipo
Mose ndi Aroni anacoka pamaso pa msonkhano kumka ku khomo la cihema
cokomanako, nagwa nkhope zao pansi; ndipo ulemerero wa Yehova
unaonekera iwo. 7Ndipo Yehova ananena ndi Mose, nati, 8Tenga ndodoyo,
nusonkhanitse khamulo; iwe ndi Aroni mbale wako, munene ndi thanthwe
pamaso pao, kuti liwapatse madzi; potero uwaturutsire madzi m'thanthwe, ndi
kumwetsa khamu la anthu ndi zoweta zao. 9Ndipo Mose anatenga ndodoyo
kuicotsa pamaso pa Yehova, monga iye anamuuza iye. 10Ndipo Mose ndi Aroni
anasonkhanitsa msonkhano pathanthwe, nanena nao iye, Tamvanitu,
opikisana naye inu; kodi tikuturutsireni madzi m'thanthwe umu? 11Ndipo Mose
anasamula dzanja lace, napanda thanthwe kawiri ndi ndodo; ndipo madzi
anaturukamo ocuruka, ndi khamulo linamwa, ndi zoweta zao zomwe. 12Ndipo
Yehova ananena ndi Mose ndi Aroni, Popeza simunandikhulupirira Ine,
kundipatula Ine pamaso pa ana a Israyeli, cifukwa cace simudzalowetsa
msonkhano uwu m'dziko ndinawapatsali. 13Awa ndi madzi a Meriba; popeza
ana a Israyeli anatsutsana ndi Yehova, ndipo anapatulidwa mwa iwowa.

Mose apempha njira kwa Aedomu

14Pamenepo Mose anatumiza amithenga ocokera ku Kadesi kumuka kwa
mfumu ya Edomu, ndi kuti, Atero mbale wanu Israyeli, Mudziwa zowawa zonse
zinatigwera; 15kuti makolo athu anatsikira kumka ku Aigupto, ndipo tinakhala
m'Aigupto masiku ambiri; ndipo Aaigupto anacitira zoipa ife, ndi makolo
athu. 16Pamenepo tinapfuulira kwa Yehova, ndipo anamva mau athu, natuma
mthenga, natiturutsa m'Aigupto; ndipo, taonani, tiri m'Kadesi, ndiwo mudzi wa
malekezero a malire anu. 17Tipitetu pakati pa dziko lanu; sitidzapitira
pamunda, kapena munda wampesa, sitidzamwa madzi a m'zitsime; tidzatsata
mseu wacifumu; sitidzapatukira kulamanja kapena kulamanzere, mpaka
titapitirira malire anu. 18Koma Edomu ananena naye, Usapitire pakati pa ine,
kuti ndingaturuke kukomana nawe ndi lupanga. 19Ndipo ana a Israyeli
ananena naye, Tidzatsata mseu; ndipo tikakamwa madzi ako, ine ndi zoweta
zanga, pamenepo ndidzapatsa mtengo wace; sindifuna kanthu kena koma
kungopitapo mwa njira. 20Koma anati, Usapitirepo. Ndipo Edomu anaturukira
kukumana naye ndi anthu ambiri, ndi dzanja lamphamvu. 21Potero Edomu
anakana kulola Israyeli kupitira pa malire ace; cifukwa cace Aisrayeli
anampatukira.

Imfa ya Aroni

22Ndipo anayenda ulendo kucokera ku Kadesi; ndi ana a Israyeli, ndilo khamu
lonse, anadza ku phiri la Hori. 23Ndipo Yehova ananena ndi Mose ndi Aroni
m'phiri la Hori, pa malire a dziko la Edomu, ndi kuti, 24Aroni adzaitanidwa
kumka kwa anthu a mtundu wace; pakuti sadzalowa m'dziko limene ndapatsa
ana a Israyeli, popeza munapikisana ndi mau anga ku madzi a
Meriba. 25Tenga Aroni ndi Eleazara mwana wace, nukwere nao m'phiri la
Hori; 26nubvule Aroni zobvala zace, numbveke Eleazara mwana wace; ndipo

Aroni adzaitanidwa kumka kwa anthu a mtundu wace, nadzafa komweko. 27Pamenepo Mose anacita monga adamuuza; ndipo anakwera m'phiri la Hori pamaso pa khamu lonse. 28Ndipo Mose anabvula Aroni zobvala zace, nabveka Eleazara mwana wace; ndipo Aroni anafa pomwepo pamwamba pa phiri, Pamenepo Mose ndi Eleazara anatsika m'phirimo. 29Pamene khamu lonse linaona kuti Aroni adamwalira, anamlira Aroni masiku makumi atatu, ndiyo mbumba yonse ya Israyeli.

Aisrayeli aononga Akanani

1Pamene Mkanani, mfumu ya Aradi, wokhala kumwela, anamva
kuti Israyeli anadzera njira ya azondi, anathira nkhondo pa Israyeli,
nagwira ena akhale ansinga. 2Ndipo Israyeli analonjeza cowinda
kwa Yehova, nati, Mukadzaperekatu anthu awa m'dzanja langa,
ndidzaononga midzi yao konse. 3Ndipo Yehova anamvera mau a
Israyeli, napereka Akanani; ndipo anawaononga konse ndi midzi
yao yomwe; nacha dzina lace la malowo Horima.

Njoka yamkuwa

4Ndipo anayenda ulendo kucokera ku phiri la Hori, nadzera njira ya
Nyanja Yofiira, kupaza ku dziko la Edomu; ndi mtima wa anthu
unada cifukwa ca njirayo. 5Ndipo anthu ananena motsutsana ndi
Mulungu, ndi Mose, ndi kuti, Mwatikwezeranji kuticotsa ku Aigupto
kuti tifere m'cipululu? pakuti mkate ndi madzi palibe, ndi mtima
wathu walema nao mkate wacabe uwu. 6Pamenepo Yehova
anatumiza njoka zamoto pakati pa anthu, ndipo zinaluma anthu;
nafapo anthu ambiri a Israyeli. 7Ndipo anthu anadza kwa Mose,
nati, Tacimwa, popeza tinanena motsutsana ndi Yehova, ndi inu;
pempherani kwa Yehova kuti aticotsere njokazi. Ndipo Mose
anawapempherera anthu. 8Pamenepo Yehova anati kwa Mose,
Upange njoka yamoto; nulike pa mtengowace; ndipo kudzali, kuti
onse olumwa, akuipenya njokayo, adzakhala ndi moyo. 9Ndipo
Mose anapanga njoka yamkuwa, naiika pamtengo; ndipo kunali,
njoka itamluma munthu ali yense, nakapenyetsetsa iye pa njoka
yamkuwa, nakhala ndi moyo.

Acoka kumka ulendo wao

10Pamenepo ana a Israyeli anayenda ulendo, namanga mahema
m'Oboti. 11Ndipo anacoka ku Oboti, namanga mahema ku
Iyebarimu, m'cipululu cakuno ca Moabu, koturukira
dzuwa. 12Pocokapo anayenda ulendo, namanga mahema m'cigwa
ca Zaredi. 13Atacokako anayenda ulendo, namanga mahema tsidya
tina la Arinoni, wokhala m'cipululu, wogwera ku malire a Aamori;
popeza Arinoni ndiwo malire a Moabu, pakati pa Moabu ndi
Aamori. 14Cifukwa cace, ananena m'buku la Nkhondo za Yehova,

Vahebi m'Sufa,
Ndi miyendo ya Arinoni;
15Ndi zigwa za miyendoyo
Zakutsikira kwao kwa Ari,
Ndi kuyandikizana ndi malire a Moabu.

16Ndipo atacokapo anamuka ku Been, ndico citsime cimene Yehova
anacinena kwa Mose, Sonkhanitsa anthu, ndipo ndidzawapatsa
madzi. 17Pamenepo Israyeli anayimba nyimbo iyi:

Tumphuka citsime iwe; mucithirire mang'ombe;

18Citsime adakumba mafumu,
Adacikonza omveka a anthu;
Atanena mlamuli, ndi ndodo zao.
Ndipo atacoka kucipululu anamuka ku Matana; 19atacoka ku
Matana ku Nahaliyeli; atacoka ku Nahaliyeli ku Bamoti; 20atacoka
ku Bamoti ku cigwa ciri m'dziko la Moabu, ku mutu wa Pisiga,
popenyana ndicipululu.
Aisrayeli alanda dziko la Aamori
21Ndipo Israyeli anatuma amithenga kwa Sihoni mfumu ya Aamori,
ndi kuti, 22Ndipitire pakati pa dziko lako; sitidzapatuka kulowa
m'munda, kapena m'munda wampesa, sitidzamwako madzi a
m'zitsime; tidzatsata mseu wacifumu, kufikira tapitirira malire
ako. 23Ndipo Sihoni sanalola Israyeli apitire m'malire ace; koma
Sihoni anamemeza anthu ace onse, nadzakomana naye Israyeli
m'cipululu, nafika ku Jahazi, nathira nkhondo pa Israyeli. 24Ndipo
Israyeli anamkantha ndi lupanga lakuthwa, nalanda dziko lace
likhale lao lao, kuyambira Arinoni kufikira Yaboki, kufikira ana ai
Amoni; popeza malire a ana a Amoni ndiwo olimba. 25Ndipo
Israyeli analanda midzi iyi yonse; nakhala Israyeli m'midzi yonse
ya Aamori; m'Hesiboni ndi miraga yace yonse. 26Popeza Hesiboni
ndiwo mudzi wa Sihoni mfumu ya Aamori, imene idathira nkhondo
pa mfumu idafayo ya Moabu, nilanda dziko lace m'dzanja lace
kufikira Arinoni. 27Cifukwa cace iwo akunena mophiphiritsa akuti,
Idzani ku Hesiboni,
Mudzi wa Sihoni umangike, nukhazikike:
28Popeza moto unaturuka m'Hesiboni,
Cirangali ca mota m'mudzi wa Sihoni;
Catha Ari wa Moabu,
Eni misanje ya Arinoni.
29Tsoka kwa iwe, Moabu!
Mwaonongeka, anthu a Kemosi inu,
Anapereka ana ace amuna opulumuka,
Ndi ana ace akazi akhale ansinga,
Kwa Sihoni mfumu ya Aamori.
30Tinawagwetsa; Hesiboni waonongeka kufikira ku Diboni,
Ndipo tinawapulululutsa kufikira ku Nofa,
Ndiwo wakufikira ku Medeba.
31Comweco Israyeli anakhala m'dziko la Aamori. 32Ndipo Mose
anatumiza anthu akazonde Yazere, nalanda miraga yace,
napitikitsa Aamori a komweko.
Aisrayeli alanda dziko la Basana
33Ndipo anatembenuka nakwera kudzera njira ya ku Basanu; ndipo
Ogi mfumu ya ku Basana anaturuka kukumana nao, iye ndi anthu
ace onse, kudzacita nao nkhondo ku Edreyi. 34Ndipo Yehova anati

kwa Mose, Usamuopa; popeza ndampereka m'manja mwako, iye ndi anthu ace onse, ndi dziko lace; umcitire monga umo unacitira Sihoni mfumu ya Aamori anakhalayo ku Hesiboni. 35Ndipo anamkantha iye, ndi ana ace amuna ndi anthu ace onse, kufikira sanatsala ndi mmodzi yense; nalanda dziko lace likhale lao lao.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Za Balamu ndi Balaki

1Ndipo ana a Israyeli anayenda ulendo, namanga mahema
m'zigwa za Moabu, tsidya la Yordano ku Yeriko.
2Ndipo Balaki mwana wa Zipori anaona zonse Israyeli anacitira
Aamori. 3Ndipo Moabu anacita mantha akuru ndi anthuwo, popeza
anacuruka; nada mtima Moabu cifukwa ca ana a Israyeli. 4Ndipo
Moabu anati kwa akuru a Midyani, Tsopano msonkhano uwu
udzanyambita zonse ziri pozinga pathu, monga ng'ombe
zinyambita msipu wa kubusa. Ndipo Balaki mwana wa Zipori anali
mfumu ya Moabu masiku amenewo. 5Ndipo anatuma amithenga
kwa Balamu mwana wa Beori, ku Petori, wokhala kumtsinje, wa
dziko la anthu a mtundu wace, kuti amuitane, ndi kuti, Taonani,
anaturuka anthu m'dziko la Aigupto; taonani, aphimba nkhope ya
dziko, nakhala popenyana ndi ine. 6Ndipo tsopano, idzatu,
nunditembererere anthu awa; popeza andiposa mphamvu; kapena
ndidzawalaka, kuti tiwakanthe, ndi kuti ndiwapitikitse m'dziko;
pakuti ndidziwa kuti iye amene umdalitsa adalitsika, ndi iye amene
umtemberera atembererereka. 7Ndipo akuru a Moabu ndi akuru a
Midyani anamuka ndi mphotho za maula m'dzanja lao; anadza kwa
Balamu, nanena naye mau a Balaki. 8Ndipo ananena nao, Mugone
kuno usiku uno, ndidzakubwezerani mau, monga Yehova adzanena
ndi ine; pamenepo mafumu a Moabu anagona ndi Balamu. 9Ndipo
Mulungu anadza kwa Balamu, nati, Anthu awa ali ndi iwe ndiwo
ayani? 10Ndipo Balamu anati kwa Mulungu, Balaki mwana wa
Zipori mfumu ya Moabu, anatumiza kwa ine, ndi kuti, 11Taonani,
anthu awa adaturuka m'Aigupto aphimba nkhope ya dziko, idzatu
unditembererere awa; kapena ndidzakhoza kulimbana nao
nkhondo, ndi kuwapitikitsa. 12Koma Mulungu anati kwa Balamu,
Usapita nao; usatemberera anthuwa; pakuti adalitsika. 13Ndipo
Balamu anauka m'mawa, nati kwa akalonga a Balaki, Mukani ku
dziko lanu; popeza Yehova andikaniza kuti ndisapite
nanu, 14Pamenepo akalonga a Moabu ananyamuka, nafika kwa
Balaki, nati, Alikukana Balamu kudza nafe. 15Koma Balaki
anaonjeza kutumanso akalonga, ocuruka, ndi omveka koposa
awa. 16Ndipo anadza kwa Balamu, nati kwa iye, Atero Balaki
mwana wa Zipori, Pasakhaletu cinthu cakukuletsa kudza kwa
ine; 17popeza ndidzakucitira ulemu waukuru, ndipo zonse unena
ndi ine ndidzacita; cifukwa cace idzatu, unditembererere anthu
awa. 18Ndipo Balamu, anayankha nati kwa anyamata a Balaki,
Cinkana Balaki andipatsa nyumba yace yodzala ndi siliva ndi golidi,
sindikhoza kutumpha mau a Yehova Mulungu wanga, kucepsako
kapena kuonjezako. 19Ndikupemphani, tsono, khalani pano inu
usiku uno womwe; kuti ndidziwe comwe Yehova adzanenanso

nane. 20Ndipo Mulungu anadza kwa Balamu usiku, nanena naye, Akadza kukuitana anthuwa, nyamuka, kumka nao, koma mau okha okha ndinena ndi iwe, ndiwo ukacite. 21Pamenepo Balamu anauka m'mawa namanga buru wace, namuka nao akalonga a ku Moabu. 22Koma anapsa mtima Mulungu cifukwa ca kupita iye, ndipo mthenga wa Yehova anadziika m'njira wotsutsana naye, Ndipo anali wokwera pa buru wace, ndi anyamata ace awiri anali naye, 23Ndipo buruyo anaona mthenga wa Yehova alikuima m'njira, ndi lupanga lace ku dzanja lace; ndi buru anapatuka m'njira, nalowa kuthengo; ndipo Balamu anampanda buru kumbwezera kunjira. 24Pamenepo mthenga wa Yehova anaima m'njira yopapatiza ya minda yampesa; mbali yina kuli linga, mbali yina linga. 25Ndipo buru anaona mthenga wa Yehova, nadzikankhira kulinga, nakanikiza phazi la Balamu kulinga; ndipo anampandanso. 26Pamenepo mthenga wa Yehova anapitiriranso, naima popapatiza, popanda popatukira kulamanja kapena kulamanzere. 27Ndipo buru wace anaona mthenga wa Yehova, nagona pansi, Balamu ali pamsana pace; ndipo Balamu adapsa mtima, nampanda buru ndi ndodo. 28Ndipo Yehova anatsegula pakamwa pace pa buru, nati uyu kwa Balamu, Ndakucitanji, kuti wandipanda katatu tsopano? 29Pamenepo Balamu anati kwa buru, Cifukwa wandipeputsa; mukadakhala lupanga m'dzanja langa tsopano, ndikadakupha iwe. 30Ndipo buru anati kwa Balamu, Si ndine buru wako amene umayenda wokwera pa ine ciyambire ndiri wako kufikira lero lino? Kodi ndikakucitira cotere ndi kale lonse? Ndipo anati, Iai. 31Pamenepo Yehova anapenyetsa maso a Balamu, naona iye mthenga wa Yehova alikuima m'njira, lupanga losolola liri kudzanja, ndipo anawerama mutu wace, nagwa nkhope yace pansi. 32Ndipo mthenga wa Yehova ananena naye, Wapandiranji buru wako katatu tsopano? taona, ndaturuka kuti nditsutsane nawe popeza njira iyi ikugwetsa camtu pamaso panga; 33koma buru anandiona, nandipatukira nthawi izi zitatu pondiona; akadapanda kundipatukira, ndikadakupha iwe ndithu, ndi kumsunga iye wamoyo. 34Pamenepo Balamu anati kwa mthenga wa Yehova, Ndacimwa, popeza sindinadziwa kuti munaima mondiletsa m'njira; ndipo tsopano, ngati cikuipirani, ndibwerera. 35Ndipo mthenga wa Yehova anati kwa Balamu, Pita nao anthuwa; koma mau okha okha ndinena ndi iwe, ndiwo ukanene, Potero Balamu anamuka nao akalonga a Balaki. 36Pamene Balaki anamva kuti wafika Balamu, anamturukira kukakomana naye ku mudzi wa Moabu, wokhala m'mphepete mwa Arinoni, ndiwo ku malekezero a malire ace. 37Ndipo Balaki anati kwa Balamu, Kodi sindinatumiza kwa iwe ndithu kukakuitana? Unalekeranji kudza kwa ine? sindikhoza kodi kukucitira

ulemu? 38Ndipo Balamu anati kwa Balaki, Taonani, ndafika kwa inu;
ngati ndiri nayo mphamvu konse tsopano kunena kanthu? mau
amene Mulungu aike m'kamwa mwanga ndiwo
ndidzanena. 39Ndipo Balamu anamuka ndi Balaki, nafika iwo ku
Kiriyati Huzoti. 40Pamenepo Balaki anapha ng'ombe ndi nkhosa,
natumizira Balamu, ndi akalonga okhala naye. 41Ndipo kunali kuti
m'mawa, Balaki anatenga Balamu, nakwera nave ku misanje ya
Baala, ndi kumeneko anaona malekezero a anthuwo.

©The Bible Society of Malawi, 1992

1Ndipo Balamu anati kwa Balaki, Ndimangireni kuno maguwa a
nsembe asanu ndi awiri, nimundikonzere kuno ng'ombe zisanu ndi
ziwiri, ndi nkhosa zamphongo zisanu ndi ziwiri. 2Ndipo Balaki
anacita monga Balamu ananena; ndipo Balaki ndi Balamu
anapereka pa guwa la nsembe liri lonse ng'ombe ndi nkhosa
yamphongo. 3Ndipo Balamu anati kwa Balaki, Imani pa nsembe
yopsereza yanu, ndipite ine, kapena Yehova akadza kukomana ndi
ine; ndipo cimene akandionetsa ine ndidzakufotokozerani. Ndipo
anapita pamsanje poyera, 4Pamenepo Mulungu anakomana ndi
Balamu; ndipo ananena ndi iye, Ndakonza maguwa a nsembe asanu
ndi awiri, ndipo ndapereka ng'ombe ndi nkhosa yamphongo pa
guwa la nsembe liri lonse. 5Ndipo Yehova anaika mau m'kamwa
mwa Balamu, nati, Bwerera kwa Balaki, nukanene cakuti
cakuti. 6Ndipo anabwerera kwa iye, ndipo, taonani, analikuima pa
nsembe yopsereza yace, iye ndi akalonga onse a Moabu. 7Ndipo
ananena fanizo lace, nati,
Ku Aramu ananditenga Balaki,
Mfumu ya Moabu ananditenga ku mapiri a kum'mawa;
Idza, udzanditembererere Yakobo.
Idza, nudzanyoze Israyeli.
8Ndidzatemberera bwanji amene Mulungu sanamtemberera?
Ndidzanyoza bwanji, amene Yehova sanamnyoza?
9Pakuti, pokhala pamwamba pa matanthwe ndimpenya,
Pokhala pa zitunda ndimuyang'ana;
Taonani, ndiwo anthu akukhala paokha.
Osadziwerengera pakati pa amitundu ena,
10Adzawerenga ndani pfumbi la Yakobo,
Kapena kuwerenga limodzi la magawo anai la Israyeli?
Ndipo ine ndife monga amafa aongoka mtima,
Citsiriziro canga cifanane naco cace!
11Pamenepo Balaki anati kwa Balamu, Wandicitiranji?
Ndinakutenga utemberere adani anga, ndipo taona, wawadalitsa
ndithu. 12Ndipo anayankha nati, Cimene aciika m'kamwa mwanga
Yehova, sindiyenera kodi kunena ici? 13Ndipo Balaki anati naye,
Tiyetu, upite nane kumalo kwina, kumene ukawaona; udzaona
malekezero ao okha, osawaona onse; ndipo pokhala pamenepo
ukanditembererere iwo. 14Ndipo anamuka naye ku thengo la
Zofimu, pamwamba pa Pisiga, namangako maguwa a nsembe
asanu ndi awiri, napereka ng'ombe ndi nkhosa pa guwa la nsembe
liri lonse. 15Ndipo anati kwa Balaki, Imani pano pa nsembe
yopsereza yanu, ndipite ine ndikakomane ndi iye uko. 16Ndipo
Yehova anakomana naye Balamu, naika mau m'kamwa mwace,
nati, Bwerera kwa Balaki, nukanene cakuti cakuti. 17Ndipo anadza

kuli iye, ndipo taona, analikuima pa nsembe yace yopsereza, ndi akalonga a Moabu pamodzi naye. Ndipo Balaki anati kwa iye, Wanenanji Yehova? 18Ndipo ananena fanizo lace, nati,
Ukani, Balaki, imvani;
Ndimvereni, mwana wa Zipori;
19Mulungu sindiye munthu, kuti aname;
Kapena mwana wa munthu, kuti aleke;
Kodi anena, osacita?
20Kapena kulankhula, osacitsimikiza?
Taonani, ndalandira mau akudalitsa,
Popeza iye wadalitsa, sinditha kusintha.
21Sayang'anira mphulupulu iri m'Yakobo,
Kapena sapenya kupulukira kuli m'Israyeli.
Yehova Mulungu wace ali ndi iye,
Ndi mpfuu wa mfumu uli pakati pao,
22Mulungu awaturutsa m'Aigupto;
Mphamvu yace ikunga ya njati.
23Pakuti palibe nyanga pakati pa Yakobo,
Kapena ula mwa Israyeli;
Pa nyengo yace adzanena kwa Yakobo ndi Israyeli,
Cimene Mulungu acita.
24Taonani, anthuwo auka ngati mkango waukazi,
Nadzitukumula ngati mkango waumuna:
Sugonansokufikira utadya nyama yogwira,
Utamwa mwazi wa zophedwa.
25Ndipo Balaki anati kwa Balamu, Usawatemberera konse, kapena kuwadalitsa konse. 26Koma Balamu anayankha nati kwa Balaki, Sindinakuuzani ndi kuti, Ciri conse acinena Yehova, comweco ndizicita? 27Ndipo Balaki anati kwa Balamu, Tiyetu, ndimuke nawe kumalo kwina; kapena kudzakomera pamaso pa Mulungu kuti unditembererere iwo pokhala kumeneko.
28Ndipo Balaki anamka naye Balamu pamwamba pa Peori, popenyana ndi cipululu. 29Ndipo Balamu anati kwa Balaki, Mundimangire pano maguwa a nsembe asanu ndi awiri, nimundikonzere pano ng'ombe zisanu ndi ziwiri, ndi nkhosa zamphongo zisanu ndi ziwiri. 30Ndipo Balaki anacita monga adanena Balamu, napereka ng'ombe ndi nkhosa yamphongo pa guwa la nsembe liri laose.

©The Bible Society of Malawi, 1992

1Pamene Balamu anaona kuti kudakomera pamaso pa Yehova
kudalitsa Israyeli, sanamuka, monga nthawi zija zina, ku nyanga
zolodzera, koma anayang'ana nkhope yace kucipululu. 2Ndipo
Balamu anakweza maso ace, naona Israyeli alikukhala monga mwa
mafuko ao; ndipo mzimu wa Mulungu unadza pa iye. 3Pamenepo
ananena fanizo lace, nati,
Balamu mwana wa Beori anenetsa,
Ndi munthuyo anatsinzina maso anenetsa;
4Wakumva mau a Mulungu anenetsa,
Wakuona masomphenya a Wamphamvuyonse,
Wakugwa pansi maso ace openyuka:
5Ha! mahema ako ngokoma, Yakobo;
Zokhalamo zako, Israyeli!
6Ziyalika monga zigwa,
Monga minda m'mphepete mwanyanja,
Monga khonje waoka Yehova,
Monga mikungudza m'mphepete mwa madzi.
7Madzi adzayenda naturuka m'zotungira zace,
Ndi mbeu zace zidzakhala ku madzi ambiri,
Ndi mfumu yace idzamveka koposa Agagi,
Ndi ufumu wace udzamveketsa.
8Mulungu amturutsa m'Aigupto;
Ali nayo mphamvu yonga ya njati;
Adzawadya amitundu, ndiwo adani ace.
Nadzaphwanya mafupa ao, Ndi kuwapyoza ndi mibvi yace.
9Anaunthama, nagona pansi ngati mkango,
Ngati mkango waukazi; adzamuutsa ndani?
Wodalitsika ali yense wakudalitsa iwe,
Wotembererekа ali yense wakutemberera iwe.
10Pamenepo Balaki anapsa mtima pa Balamu, naomba m'manja;
ndipo Balaki anati kwa Balamu, Ndinakuitana kutemberera adani
ansa, ndipo unawadalitsa ndithu katatu tsopano. 11Cifukwa cace
thawira ku malo ako tsopano; ndikadakucitira ulemu waukuru;
koma, taona, Yehova wakuletsera ulemu. 12Ndipo Balamu anati
kwa Balaki, Kodi sindinauzanso amithenga anu amene
munawatumiza kwa ine, ndi kuti, 13Cinkana Balaki akandipatsa
nyumba yace yodzala ndi siliva ndi golidi, sindikhoza kutumpha
mau a Yehova, kucita cokoma kapena coipa ine mwini wace;
conena Yehova ndico ndidzanena ine? 14Ndipo tsopano, taonani,
ndimuka kwa anthu a mtundu wanga; tiyeni, ndidzakulangizani,
ndi kukuuzani zimene anthu awa adzacitira anthu anu, masiku
otsiriza. 15Ndipo ananena fanizo lace, nati,
Balamu mwana wa Beori anenetsa,

Ndi munthu wotsinzina masoyo anenetsa;
16Anenetsa wakumva mau a Mulungu,
Ndi kudziwa nzeru ya Wam'mwambamwamba,
Wakuona masomphenya a Wamphamvuyonse,
Wakugwa pansi wopenyuka maso;
17Ndimuona, koma tsopano ai; Ndimpenya, koma si pafupi ai;
Idzaturuka nyenyezi m'Yakobo,
Ndi ndodo yacifumu idzauka m'Israyeli,
Nidzakantha malire a Moabu,
Nidzapasula ana onse a Seti,
18Ndi Edomu adzakhala ace ace,
Seiri lomwe lidzakhala lace lace, ndiwo adani ace;
19Koma Israyeli adzacita zamphamvu.
Ndipo wina woturuka m'Yakobo adzacita ufumu;
Nadzapasula otsalira m'mudzi.
20Ndipo anayang'ana ku Amaleki, nanena fanizo lace, nati,
Amaleki ndiye woyamba wa amitundu;
Koma citsiriziro cace, adzaonongeka ku nthawi zonse.
21Ndipo anayang'ana Akeni, nanena fanizo lace, nati,
Kwanu nkokhazikika,
Wamanga cisa cako m'thanthwe.
22Koma Kaini adzaonongeka,
Kufikira Asuri adzakumanga nsinga.
23Ndipo ananena fanizo lace, nati,
Ha! adzakhala ndi moyo ndani pakucita ici Mulungu?
24Koma zombo zidzafika kucokera ku doko la Kitimu,
Ndipo adzasautsa Asuri, nadzasautsa Ebere,
Koma iyenso adzaonongeka.
25Ndipo Balamu anauka, namuka nabwerera kumalo kwace; ndi
Balaki yemwe anamka njira yace.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Aisrayeli acita cigololo napembedza mafano ku Sitimu

1Ndipo Israyeli anakhala m'Sitimu, ndipo anthu anayamba kucita
cigololo ndi ana akazi a Moabu; 2popeza anaitana anthuwo adze ku
nsembe za milungu yao; ndipo anthuwo anadya, nagwadira
milungu yao. 3Pamene Israyeli anaphatikana ndi Baala Peori,
Mulungu anapsa mtima pa Israyeli. 4Ndipo Yehova anati kwa Mose,
Gwira akuru onse a anthu nuwapacikire Yehova, pali dzuwa poyera,
kuti mkwiyo waukali wa Yehova ucoke kwa Israyeli. 5Ndipo Mose
anati kwa oweruza a Israyeli, Iphani, yense anthu ace
adapatikanawo ndi Baala-Peori. 6Ndipo, taonani, anadza wina wa
ana a Israyeli, nabwera naye mkazi Mmidyani kudza naye kwa
abale ace, pamaso pa Mose, ndi pamaso pa khamu lonse la ana a
Israyeli, pakulira iwo pa khomo la cihema cokomanako. 7Pamene
Pinehasi mwana wa Eleazara, mwana wa Aroni wansembe,
anaciona, anauka pakati pa khamu, natenga nthungo m'dzanja
lace; 8natsata munthu M-israyeli m'hema, nawamoza onse awiri,
munthu M-israyeli ndi mkaziyo m'mimba mwace. Pamenepo mliri
unaletseka kwa ana a Israyeli. 9Ndipo akufa nao mliri ndiwo zikwi
makumi awiri ndi zinai.
10Ndipo Yehova ananena ndi Mose, nati, 11Pinehasi mwana wa
Eleazara, mwana wa Aroni wansembe, wabweza kuzaza kwanga pa
ana a Israyeli, popeza anacita nsanje ndi nsanje yanga pakati pao,
kotero kuti sindinawatha ana a Israyeli m'nsanje yanga. 12Cifukwa
cace nena, Taonani, ndimpatsa iye pangano langa la
mtendere; 13ndipo lidzakhala kwa iye, ndi kwa mbeu zace
zakumtsata pangano la unsembe wosatha, popeza anacita nsanje
cifukwa ca Mulungu wace, anawacitira ana a Israyeli
cowatetezera. 14Koma dzina la M-israyeli adamuphayo, ndiye
amene adamupha pamodzi ndi mkazi Mmidyani, ndiye Zimiri
mwana wa Salu, mfumu ya nyumba va makolo mwa
Asimeoni. 15Ndi dzina la mkazi Mmidyani adamuphayo ndiye Kozibi
mwana wamkazi wa Zuri; ndiye mkuru wa anthu a nyumba ya
makolo m'Midyani.
16Ndipo Yehova ananena ndi Mose, ndi kuti, 17Sautsa Amidyani ndi
kuwakantha; 18popeza akusautsani ndi manyengo ao amene
anakunyengani nao; m'cija ca Peori, ndi ca Kozibi, mwana wamkazi
wa kalonga wa ku Midyani, mlongo wao, amene adamupha tsiku la
mliri, m'cija ca Peori.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Awerenzedwa Aisrayeli

1Ndipo kunali, utatha mliriwo, Yehova ananena ndi Mose ndi
Eleazara mwana wa Aroni wansembe, nati, 2Werenga khamu lonse
la ana a Israyeli, kuyambira a zaka makumi awiri ndi mphambu,
monga mwa nyumba za makolo ao, onse akuturukira kunkhondo
m'Israyeli. 3Pamenepo Mose ndi Eleazara wansembe ananena nao
m'zidikha za Moabu pa Yordano kufupi ku Yeriko, ndi
kuti, 4Awawerenge kuyambira a zaka makumi awiri ndi mphambu;
monga Yehova anawauza Mose ndi ana a Israyeli, amene
adaturuka m'dziko la Aigupto.
5Rubeni, ndiye woyamba kubadwa wa Israyeli; ana amuna a
Rubeni ndiwo: Hanoki, ndiye kholo la banja la Ahanoki; Palu, ndiye
kholo la banja la Apalu; 6Hezeroni, ndiye kholo la banja la
Ahezeroni; Karimi, ndiye kholo la banja la Akarimi. 7Iwo ndiwo
mabanja a Arubeni; owerengedwa ao ndiwo zikwi makumi anai
mphambu zitatu kudza mazana asanu ndi awiri mphambu makumi
atatu, 8Mwana wamwamuna wa Palu ndiye Eliyabu. 9Ndi ana a
Eliyabu: Nemueli, ndi Datani ndi Abiramu. Iwo ndiwo Datani ndi
Abiramu omwe aja oitanidwa a khamu, amene anatsutsana ndi
Mose ndi Aroni mu msonkhano wa Kora, mula anatsutsana ndi
Yehova; 10ndipo dziko linayasama pakamwa pace, ndi kuwameza
pamodzi ndi Kora, pakufa msonkhano uja; muja mote unaononga
amuna mazana awiri ndi makumi asanu, nakhala iwo
cizindikilo. 11Koma sanafa ana amuna a Kora.
12Ana amuna a Simeoni monga mwa mabanja ao ndiwo: Nemueli,
ndiye kholo la banja la Anemueli; Yamini, ndiye kholo la banja la
Ayamini; Yakini, ndiye kholo la banja la Ayakini; 13Zera, ndiye kholo
la banja la Azera; Sauli, ndiye kholo la banja la Asauli. 14Iwo ndiwo
mabanja a Asimeoni, zikwi makumi awiri mphambu
ziwirikudzamazana awiri.
15Ana amuna a Gadi monga mwa mabanja ao ndiwo: Zefoni, ndiye
kholo la banja la Azefoni; Hagi, ndiye kholo la banja la Ahagi; Suni,
ndiye kholo la banja la Asuni; 16Ozini, ndiye kholo la banja la
Aozini; Eri, ndiye kholo la banja la Aeri; 17Arodi, ndiye kholo la
banja la Aarodi; Areli, ndiye kholo la banja la Aareli. 18Iwo ndiwo
mabanja a ana a Gadi, monga mwa owerengedwa ao, zikwi
makumi anai ndi mazana asanu.
19Ana amuna a Yuda, ndiwo Eri ndi Onani; ndipo Eri ndi Onani
anamwalira m'dziko la Kanani. 20Ndipo ana a Yuda monga mwa
mabanja ao ndiwo: Sela, ndiye kholo la banja la Asela; Perezi,
ndiye kholo la banja la Aperezi; Zera, ndiye kholo la banja la
Azera. 21Ndipo ana a Perezi ndiwo: Hezeroni, ndiye kholo la banja
la Ahezeroni; Hamuli, ndiye kholo la banja la Ahamuli. 22Iwo ndiwo

mabanja a Yuda monga mwa owerengedwa ao, zikwi makumi asanu ndi awiri mphambu zisanu ndi cimodzi kudza mazana asanu.
23Ana amuna a Isakara monga mwa mabanja ao ndiwo: Tola, ndiye kholo la banja la Atola; Puva, ndiye kholo la banja la
Apuni; 24Yasubi, ndiye kholo la banja la Ayasubi; Simironi, ndiye kholo la banja la Asimironi. 25Iwo ndiwo mabanja a Isakara monga mwa owerengedwa ao; zikwi makumi asanu ndi limodzi mphambu zinai kudza mazana atatu.
26Ana amuna a Zebuloni monga mwa mabanja ao ndiwo: Seredi, ndiye kholo la banja la Aseredi; Eloni, ndiye kholo la banja la Aeloni; Yahaliyeli, ndiye kholo la banja la Ayahaliyeli. 27Iwo ndiwo mabanja a Zebuloni monga mwa owerengedwa ao, zikwi makumi asanu ndi limodzi mphambu mazana asanu.
28Ana amuna a Yosefe monga mwa mabanja ao ndiwo: Manase ndi Efraimu. 29Ana a Manase ndiwo: Makiri, ndiye kholo la banja la Amakiri; ndipo Makiri anabala Gileadi; ndiye kholo la banja la Agileadi, 30Ana a Gileadi ndiwo: Yezeri, ndiye kholo la banja la Ayezeri; Heleki, ndiye kholo la banja la Aheleki; 31ndi Asiriyeli, ndiye kholo la banja la Aasiriyeli; ndi Sekemu, ndiye kholo la banja la Asekemu; 32ndi Semida, ndiye kholo la banja la Asemida; ndi Heferi, ndiye kholo la banja la Aheferi. 33Ndipo Tselofekadi mwana wa Heferi analibe ana amuna, koma ana akazi ndiwo; ndipo maina a ana akazi a Tselofekadi ndiwo Mala ndi Nowa, Hogila, Milika ndi Tiriza. 34Iwo ndiwo mabanja ao a Manase; ndipo owerengedwa ao ndiwo zikwi makumi asanu mphambu ziwiri kudza mazana asanu ndi awiri.
35Ana amuna a Efraimu monga mwa mabanja ao ndiwo: Sutela, ndiye kholo la banja la Asutela; Bekeri, ndiye kholo la banja la Abekeri; Tahana, ndiye kholo la banja la Atahana. 36Ndipo mwana wamwamuna wa Sutela ndiye Erani, ndiye kholo la banja la Aerani. 37Iwo ndiwo mabanja a ana a Efraimu monga mwa owerengedwa ao, ndiwo zikwi makumi atatu mphambu ziwiri kudza mazana asanu. Iwo ndiwo ana amuna a Yosefe monga mwa mabanja ao.
38Ana amuna a Benjamini monga mwa mabanja ao ndiwo: Bela, ndiye kholo la banja la Abela; Asibeli, ndiye kholo la banja la Aasibeli; Ahiramu, ndiye kholo la banja la Aahiramu; 39Sufamu ndiye kholo la banja la Asufamu; Hufamu, ndiye kholo la banja la Ahufamu. 40Ndipo ana amuna a Bela ndiwo Aridi ndi Namani; Aridi, ndiye kholo la banja la Aaridi; Namani, ndiye kholo la banja la Anamani. 41Iwo ndiwo ana a Benjamini monga mwa mabanja ao; ndipo owerengedwa ao ndiwo zikwi makumi anai mphambu zisanu kudza mazana asanu ndi limodzi.

42Mwana wamwamuna wa Dani monga mwa mabanja ace ndiye
Suhamu, ndiye kholo la banja la Asuhamu. Iwo ndiwo mabanja a
Dani monga mwa mabanja ao. 43Mabanja aose a Asuhamu monga
mwa owerengedwa ao ndiwo zikwi makumi asanu ndi limodzi
mphambu zinai kudza mazana anai.
44Ana amuna a Aseri monga mwa mabanja ao ndiwo: Yimna, ndiye
kholo la banja la Ayimna; Yisivi, ndiye kholo la banja la Ayisivi;
Beriya, ndiye kholo la banja la Aberiya. 45Ana a Beriya ndiwo:
Heberi, ndiye kholo la banja la Aheberi; Malikiyeli, ndiye kholo la
banja la Amalikiyeli. 46Ndipo dzina la mwana wamkazi wa Aseri
ndiye Sera. 47Iwo ndiwo mabanja a ana amuna a Aseri monga mwa
owerengedwa ao, zikwi makumi asanu mphambu zitatu kudza
mazana anai.
48Ana amuna a Nafitali monga mwa mabanja ao ndiwo: Yazeli,
ndiye kholo la banja la Ayazeli; Guni, ndiye kholo la banja la
Aguni; 49Yezeri, ndiye kholo la banja la Ayezeri; Silemu, ndiye kholo
la banja la Asilemu. 50Iwo ndiwo mabanja a Nafitali, monga mwa
mabanja ao; ndipo owerengedwa ao ndiwo zikwi makumi anai
mphambu zisanu kudza mazana anai.
51Iwo ndiwo owerengedwa ao a ana a Israyeli, zikwi mazana asanu
ndi limodzi mphambu cimodzi kudza mazana asanu ndi awiri
mphambu makumi atatu.

Magawidwe a dziko

52Ndipo Yehova ananena ndi Mose, ndi kuti, 53Dziko ligawikire
iwowa monga mwa kuwerenga kwa maina, likhale colowa
cao. 54Ocurukawo, uwacurukitsire colowa cao; ocepawo
uwacepetsere colowa cao; ampatse yense colowa cace monga
mwa owerengedwa ace. 55Koma aligawe ndi kucita maere; colowa
cao cikhale monga mwa maina a mafuko a makolo ao, 56Agawire
ocuruka ndi ocepa colowa cao monga mwa kucita maere.
57Ndipo awa ndi owerengedwa ao a Alevi monga mwa mabanja ao:
Gerisoni, ndiye kholo la banja la Agerisoni; Kohati, ndiye kholo la
banja la Akohati; Merari, ndiye kholo la banja la Amerari. 58Awa ndi
mabanja a Alevi: banja la Alibini, banja la Ahebroni, banja la Amali,
banja la Amusi, banja la Akohati. Ndipo Kohati anabala
Amiramu. 59Ndipo dzina lace la mkazi wace wa Amiramu ndiye
Yokebedi, mwana wamkazi wa Levi, wobadwira Levi m'Aigupto;
ndipo iye anambalira Amiramu Aroni ndi Mose, ndi Miriamu mlongo
wao. 60Ndipo Nadabu ndi Abihu, Eleazara ndi Itamara anabadwira
Aroni. 61Koma Nadabu ndi Abihu adafa, muja anabwera nao moto
wacilendo pamaso pa Yehova. 62Ndipo owerengedwa ao ndiwo
zikwi makumi awiri mphambu zitatu, mwamuna yense wa mwezi
umodzi ndi mphambu; popeza sanawerengedwa pakati pa ana a
Israyeli; cifukwa sanawapatsa colowa mwa ana a Israyeli.

63Iwo ndiwo amene anawerengedwa ndi Mose ndi Eleazara
wansembe, amene anawerenga ana a Israyeli m'zidikha za Moabu
ku Yordano pafupi pa Yeriko. 64Koma pakati pao panalibe mmodzi
wa iwo amene anawerengedwa ndi Mose ndi Aroni wansembe,
amene anawerenga ana a Israyeli m'cipululu ca Sinai. 65Popeza
Yehova adanena za iwowa, Adzafatu m'cipululu. Ndipo sanatsalira
mmodzi wa iwowa koma Kalebi mwana wa Yefune, ndi Yoswa
mwana wa Nuni.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Ana akazi a Tselofekadi

1Pamenepo anayandikiza ana akazi a Tselofekadi mwana wa
Heferi, ndiye mwana wa Gileadi, ndiye mwana wa Makiri, ndiye
mwana wamwamuna wa Manase, wa mabanja a Manase mwana
wa Yosefe; ndipo maina a ana ace akazi ndiwo, Mala, Nowa, Hogila
ndi Milika ndi Tiriza. 2Ndipo anaima pamaso pa Mose, ndi pamaso
pa Eleazara wansembe, ndi pamaso pa akalonga, ndi khamu lonse,
pakhomo pa cihema cokomanako, ndi kuti, 3Atate wathu
adamwalira m'cipululu, ndipo sanakhala iye pakati pa msonkhano
wa iwo akusonkhana kutsutsana ndi Yehova, mu msonkhano wa
Kora; koma anafera zoipa zace zace; ndipo analibe ana
amuna. 4Licotsedwerenji dzina la atate wathu pakati pa banja lace,
popeza alibe mwana wamwamuna? Tipatseni dziko lathu lathu
pakati pa abale a atate wathu. 5Ndipo Mose anapita nao mlandu
wao pamaso pa Yehova. 6Ndipo Yehova ananena ndi Mose,
nati, 7Ana akazi a Tselofekadi anena zaona; uwapatse ndithu
colowa cikhale cao cao pakati pa abale a atate wao; nuwalandiritse
colowa ca atate wao. 8Ndipo unene ndi ana a Israyeli, ndi kuti,
Akafa munthu wamwamuna wopanda mwana wamwamuna,
colowa cace acilandire mwana wace wamkazi. 9Ndipo akapanda
kukhala naye mwana wamkazi, mupatse abale ace colowa
cace. 10Ndipo akapanda kukhala nao abale, mupatse abale a atate
wace colowa cace. 11Ndipo akapanda abale a atate wace, mupatse
wa cibale cace woyandikizana naye wa pfuko lace colowa cace,
likhale lace lace; ndipo likhale kwa ana a Israyeli lemba monga
Yehova wamuuza Mose.

Aikidwa Yoswa mmalo mwa Mose

12Ndipo Yehova anati kwa Mose, Kwera m'phiri ili la Abarimu,
nupenye dziko limene ndapatsa ana a Israyeli, 13Utaliona iwenso
udzaitanidwa kumka kwa anthu a mtundu wako, monga
anaitanidwa Aroni mbale wako; 14popeza munapikisana nao mau
anga m'cipululu ca Zini, potsutsana nane khamulo, osandipatula
Ine pa madziwo pamaso pao. Ndiwo madzi a Meriba m'Kadesi,
m'cipululu ca Zini. 15Ndipo Mose ananena ndi Yehova,
nati, 16Yehova, Mulungu wa mizimu ya anthu onse, aike munthu pa
khamulo, 17wakuturuka pamaso pao, ndi kulowa pamaso pao,
wakuwaturutsa ndi kuwalowetsa; kuti khamu la Ambuye lisakhale
ngati nkhosa zopanda mbusa. 18Ndipo Yehova anati kwa Mose,
Utenge Yoswa mwana wa Nuni, ndiye munthu mwa iye muli
mzimu, nuike dzanja lako pa iye; 19numuimike pamaso pa Eleazara
wansembe, ndi pamaso pa khamu lonse; numlangize pamaso
pao. 20Ndipo umuikirepo ulemerero wako, kuti khamu lonse la ana
a Israyeli ammvere. 21Ndipo aime pamaso pa Eleazara wansembe,

amene amfunsire monga mwa ciweruzo ca Urimu pamaso pa Yehova; ponena iye azituruka, ndi ponena iye azilowa, ndi iye ndi ana onse a Israyeli pamodzi naye, ndiwo khamu lonse. 22Ndipo Mose anacita monga Yehova adamuuza; natenga Yoswa namuimitsa pamaso pa Eleazara wansembe, ndi pamaso pa khamu lonse; 23namuikira manja ace, namlangiza monga Yehova adanena ndi dzanja la Mose.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Nsembe yopsereza yosalekeza

1Ndipo Yehova ananena ndi Mose, nati, 2Uza ana a Israyeli, nuti nao, Muzisamalira kubwera naco kwa Ine copereka canga, cakudya canga ca nsembe zanga zamoto, ca pfungo lokoma, pa nyengo yace yoikika. 3Ndipo unene nao, Nsembe yamoto imene muzibwera nayo kwa Yehova ndiyi: ana a nkhosa awiri a caka cimodzi opanda cirema, tsiku ndi tsiku, nsembe yamoto yosalekeza. 4Mwana wa nkhosa mmodziyo umpereke m'mawa, ndi mwana wa nkhosa winayo umpereke madzulo; 5ndi limodzi la magawo khumi la efa wa ufa wosalala ukhale nsembe yaufa, wosanganiza ndi limodzi la magawo anai la bini wa mafuta opera. 6Ndiyo nsembe yopsereza kosalekeza, yoikika ku phiri la Sinai, icite pfungo lokoma, nsembe yamoto ya Yehova. 7Ndi nsembe yace yothira ya mwana wa nkhosa mmodziyo ndiyo limodzi la magawo anai la bini; m'malo opatulika uthirire Yehova nsembe yothira ya cakumwa colimba. 8Ndi mwana wa nkhosa winayo umpereke madzulo; monga nsembe yaufa ya m'mawa, ndi nsembe yothira yace, umpereke; ndiyo nsembe yamoto ya pfungo lokoma la Yehova.

Nsembe yopsereza ya pa dzuwa la Sabata

9Ndipo dzuwa la Sabata ana a nkhosa awiri a caka cimodzi, opanda cirema, ndi awiri a magawo khumi a efa wa ufa wosalala, ukhale nsembe yaufa, wosanganiza ndi mafuta, ndi nsembe yace yothira; 10ndiyo nsembe yopsereza ya dzuwa la Sabata liri lonse, pamodzi ndi nsembe yopsereza yosalekeza, ndi nsembe yace yothira.

11Ndipo poyamba miyezi yanu muzibwera nayo nsembe yopsereza ya Yehova: ng'ombe zamphongo ziwiri, ndi nkhosa yamphongo imodzi, ndi ana a nkhosa asanu ndi awiri a caka cimodzi opanda cirema; 12ndi atatu a magawo khumi a efa wa ufa wosalala, ukhale nsembe yaufa, wosanganiza ndi mafuta, ndiwo wa ng'ombe iri yonse; ndi awiri a magawo khumi a ufa wosalala, ukhale nsembe yaufa, wosanganiza ndi mafuta, ndiwo wa nkhosa yamphongo imodziyo; 13ndi limodzi la magawo khumi la ufa wosalala wosanganiza ndi mafuta, ukhale nsembe yaufa, ndiwo wa mwana wa nkhosa yense; ndiyo nsembe yopsereza ya pfungo lokoma, nsembe yamoto ya. Yehova. 14Ndipo nsembe zace zothira ndizo: limodzi la magawo khumi la bini wa vinyo ndiwo wa ng'ombe imodzi, ndi limodzi la magawo atatu la hini likhale la nkhosa yamphongo, ndi limodzi la magawo anai a hini likhale la mwana wa nkhosa; ndiyo nsembe yopsereza ya mwezi uli wonse kunena miyezi yonse ya caka. 15Ndi tonde mmodzi, akhale nsembe

yaucimo ya Yehova; aikonze pamodzi ndi nsembe yopsereza
yosalekeza, ndi nsembe yace yothira.

Za madyerero omveka

16Ndipo mwezi woyamba, tsiku lakhumi ndi cinai la mwezi, pali
paskha wa Yehova. 17Ndipo tsiku lakhumi ndi cisanu la mwezi uwu
pali madyerero; masiku asanu ndi awiri azidya mkate wopanda
cotupitsa. 18Tsiku loyamba pali kusonkhana kopatulika;
musamacita nchito ya masiku ena; 19koma mubwere nayo nsembe
yamoto, nsembe yopsereza ya Yehova; ng'ombe ziwiri zamphongo,
ndi nkhosa yamphongo imodzi, ndi ana a nkhosa asanu ndi awiri a
caka cimodzi; akhale kwa inu opanda cirema; 20ndi nsembe yao ya
ufa wosalala wosanganiza ndi mafuta; mupereke atatu a magawo
khumi akhale a ng'ombe, ndi awiri a magawo khumi akhale a
nkhosa yamphongo; 21upereke limodzi la magawo khumi likhale la
mwana wa nkhosa mmodzi; uzitero ndi ana a nkhosa asanu ndi
awiri; 22ndi tonde mmodzi akhale nsembe yaucimo, yakutetezera
inu. 23Mupereke izi pamodzi ndi nsembe yopsereza ya m'mawa,
ndiyo ya nsembe yopsereza kosalekeza. 24Momwemo mupereke
cakudya ca nsembe yamoto ca pfungo lokoma la Yehova, tsiku ndi
tsiku, masiku asanu ndi awiri, cakupereka pamodzi ndi nsembe
yopsereza yosalekeza, ndi nsembe yace yothira. 25Ndipo tsiku
lacisanu ndi ciwiri mukhale nako kusonkhana kopatulika;
musamacita nchito ya masiku ena.
26Momwemonso tsiku la zipatso zoyamba, pobwera nayo nsembe
ya ufa watsopano kwa Yehova, m'madyerero anu a masabata,
muzikhala nako kusonkhana kopatulika; musamacita nchito ya
masiku ena. 27Pamenepo muzipereka nsembe yopsereza ya pfungo
lokoma kwa Yehova; ng'ombe zamphongo ziwiri, nkhosa
yamphongo imodzi, ana a nkhosa asanu ndi awiri a caka
cimodzi; 28ndi nsembe yace ya ufa wosalala wosanganiza ndi
mafuta, atatu a magawo khumi akhale a ng'ombe imodzi, awiri a
magawo khumi akhale a nkhosa yamphongo imodzi, 29limodzi la
magawo khumi likhale la mwana wa nkhosa mmodzi, momwemo
ndi ana a nkhosa asanu ndi awiri; 30tonde mmodzi wakutetezera
inu. 31Mupereke izi pamodzi ndi nsembe yopsereza yosalekeza, ndi
nsembe yace yaufa, zikhale kwa inu zopanda cirema, ndi nsembe
zace zothira.

©The Bible Society of Malawi, 1992

1Ndipo mwezi wacisanu ndi ciwiri, tsiku loyamba la mweziwo,
muzikhala nako kusonkhana kopatulika; musamacita nchito ya
masiku ena; likukhalireni inu tsiku lakuliza malipenga. 2Pamenepo
muzipereka nsembeyopsereza ya pfungo lokoma kwa Yehova;
ng'ombe imodzi yamphongo, nkhosa yamphongo imodzi, ana a
nkhosa asanu ndi awiri a caka cimodzi opanda cirema; 3ndi nsembe
yao yaufa, ufa wosalala wosanganiza ndi mafuta, atatu a magawo
khumi akhale a ng'ombeyo, awiri a magawo khumi akhale a nkhosa
yamphongo, 4ndi limodzi la magawo khumi likhale la mwana wa
nkhosa mmodzi, momwemo ndi ana a nkhosa asanu ndi awiri; 5ndi
tonde mmodzi wa nsembe yaucimo, yakutetezera inu; 6pamodzi ndi
nsembe yopsereza ya pamwezi, ndi nsembe yace yaufa, ndi
nsembe yopsereza yosalekeza, ndi nsembe yace yaufa, ndi nsembe
zace zothira, monga mwa lemba lace, zikhale za pfungo lokoma,
nsembe yamoto ya Yehova.
7Ndipo tsiku la khumi la mwezi wacisanu ndi ciwiri uwu muzikhala
nako kusonkhana kopatulika; pamenepo mudzicepetse;
musamagwira nchito; 8koma mubwere nayo nsembe yopsereza
kwa Yehova, ya pfungo lokoma; ng'ombe yamphongo imodzi,
nkhosa yamphongo imodzi, ana a nkhosa asanu ndi awiri a caka
cimodzi; akhale kwa inu opanda cirema; 9ndi nsembe yao ya ufa
wosalala wosanganiza ndi mafuta, atatu a magawo khumi akhale a
ng'ombe, awiri a magawo khumi akhale a nkhosa yamphongo
imodziyo; 10limodzi la magawo khumi likhale la mwana wa nkhosa
mmodzi, momwemo ndi ana a nkhosa asanu ndi awiri; 11tonde
mmodzi akhale nsembe yaucimo, pamodzi ndi nsembe yaucimo
yotetezera, ndi nsembe yopsereza yosalekeza, ndi nsembe yace
yaufa, ndi nsembe zace zothira.
12Ndipo tsiku lakhumi ndi cisanu la mwezi wacisanu ndi ciwiri
muzikhala nako kusonkhana kopatulika; musamacita nchito ya
masiku ena, koma mucitire Yehova madyerero masiku asanu ndi
awiri; 13ndipo mubwere nayo nsembe yopsereza, ndiyo nsembe
yamoto, ya pfungo lokoma kwa Yehova: ng'ombe zamphongo
khumi ndi zitatu, nkhosa zamphongo ziwiri, ana a nkhosa khumi
ndi anai, a caka cimodzi, akhale opanda cirema; 14ndi nsembe
yace yaufa wosalala wosanganiza ndi mafuta, atatu a magawo
khumi akhale a ng'ombe imodzi, momwemo nazo ng'ombe khumi
ndi zitatuzo, awiri a magawo khumi akhale a nkhosa yamphongo
imodzi, momwemo nazo nkhosa zamphongo ziwirizo; 15ndi limodzi
la magawo khumi likhale la mwana wa nkhosa mmodzi, momwemo
nao ana a nkhosa khumi ndi anai; 16ndi tonde mmodzi akhale
nsembe yaucimo; pamodzi ndi nsembe yopsereza yosalekeza,
nsembe yace yaufa, ndi nsembe yace yothira.

17Ndipo tsiku laciwiri muzibwera nazo ng'ombe zamphongo khumi
ndi ziwiri, nkhosa zamphongo ziwiri, ana a nkhosa khumi ndi anai a
caka cimodzi, opanda cirema; 18ndi nsembe yace yaufa, ndi
nsembe zace zothira, za ng'ombe, za nkhosa zamphongo, ndi za
ana a nkhosa, monga mwa kuwerenga kwace, ndi kutsata lemba
lace; 19ndi tonde mmodzi akhale nsembe yaucimo; pamodzi ndi
nsembe yopsereza yosalekeza, ndi nsembe yace yaufa, ndi
nsembe zace zothira.
20Ndi tsiku lacitatu ng'ombe khumi ndi imodzi, nkhosa zamphongo
ziwiri, ana a nkhosa khumi ndi anai a caka cimodzi opanda
cirema; 21ndi nsembe yace yaufa, ndi nsembe zace zothira za
ng'ombe, za nkhosa zamphongo, ndi za ana a nkhosa monga mwa
kuwerenga kwace, ndi kutsata lemba lace; 22ndi tonde mmodzi
akhale nsembe yaucimo; pamodzi ndi nsembe yopsereza
yosalekeza, ndi nsembe yace yaufa, ndi nsembe yace yothira.
23Ndi tsiku lacinai ng'ombe khumi, nkhosa zamphongo ziwiri, ana a
nkhosa khumi ndi anai, a caka cimodzi, opanda cirema; 24nsembe
yace yaufa, ndi nsembe zace zothira za ng'ombe, za nkhosa
zamphongo, ndi za ana a nkhosa, monga mwa kuwerenga kwace,
ndi kutsata lemba lace; 25ndi tonde mmodzi akhale nsembe
yaucimo; pamodzi ndi nsembe yopsereza yosalekeza, nsembe
yace yaufa, ndi nsembe yace yothira.
26Ndi tsiku lacisanu ng'ombe zisanu ndi zinai, nkhosa zamphongo
ziwiri, ana a nkhosa khumi ndi anai, a caka cimodzi, opanda
cirema; 27ndi nsembe yace yaufa, ndi nsembe zace zothira, za
ng'ombe, za nkhosa zamphongo, ndi za ana a nkhosa, monga mwa
kuwerenga kwace, ndi kutsata lemba lace; 28ndi tonde mmodzi
akhale nsembe yaucimo; pamodzi ndi nsembe yopsereza
yosalekeza, ndi nsembe yace yaufa, ndi nsembe yace yothira.
29Ndi tsiku lacisanu ndi cimodzi ng'ombe zisanu ndi zitatu, nkhosa
zamphongo ziwiri, ana a nkhosa khumi ndi anai, a caka cimodzi,
opanda cirema; 30ndi nsembe yace yaufa, ndi nsembe zace
zothira, za ng'ombe, za nkhosa zamphongo, ndi za ana a nkhosa,
monga mwa kuwerenga kwace, ndi kutsata lemba lace; 31ndi
tonde mmodzi akhale nsembe yaucimo; pamodzi ndi nsembe
yopsereza yosalekeza, nsembe yace yaufa, ndi nsembe yace
yothira.
32Ndi tsiku lacisanu ndi ciwiri ng'ombe zisanu ndi ziwiri, nkhosa
zamphongo ziwiri, ana a nkhosa khumi ndi anai, a caka cimodzi,
opanda cirema; 33ndi nsembe yace yaufa, ndi nsembe zace
zothira, za ng'ombe, za nkhosa yamphongo, ndi za ana a nkhosa,
monga mwa kuwerenga kwace, ndi kutsata lemba lace; 34ndi
tonde mmodzi akhale nsembe yaucimo; pamodzi ndi nsembe

yopsereza yosalekeza, nsembe yace yaufa, ndi nsembe yace yothira.
35Tsiku lacisanu ndi citatu muzikhala nalo tsiku loletsa;
musamacita nchito ya masiku ena; 36koma mubwere nayo nsembe
yopsereza ndiyo nsembe yamoto, ya pfungo lokoma kwa Yehova:
ng'ombe imodzi, nkhosa yamphongo imodzi, ana a nkhosa asanu
ndi awiri, a caka cimodzi, opanda cirema; 37nsembe yace yaufa,
ndi nsembe zace zothira za ng'ombe, za nkhosa zamphongo, ndi
za ana a nkhosa, monga mwa kuwerenga kwace, ndi kutsata
lemba lace; 38ndi tonde mmodzi wa nsembe yaucimo; pamodzi ndi
nsembe yopsereza yosalekeza, ndi nsembe yace yaufa, ndi
nsembe yace yothira.
39Izi muzikonzera Yehova mu nyengo zanu zoikika, pamodzi ndi
zowinda zanu, ndi zopereka zanu zaufuru, za nsembe zanu
zopsereza, ndi za nsembe zanu zaufa, ndi za nsembe zanu zothira,
ndi za nsembe zanu zoyamika. 40Ndipo Mose ananena ndi ana a
Israyeli monga mwa zonse Yehova adamuuza Mose.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Za cowinda cocita akazi

1Ndipo Mose ananena ndi akuru a mapfuko a ana a Israyeli, nati,
Cinthu anacilamulira Yehova ndi ici: 2Munthu akacitira
Yehovacowinda, kapena akalumbira lumbiro ndi kumangira moyo
wace codziletsa, asaipse mau ace; azicita monga mwa zonse
zoturuka m'kamwa mwace. 3Ndipo mkazi akacitira Yehova
cowinda, nakadzimanga naco codziletsa, pokhala ali m'nyumba ya
atate wace, m'unamwali; 4ndipo atate wace akamva cowinda cace,
ndi codziletsa cace anamanga moyo wace naco, koma wakhala
naye cete atate wace; pamenepo zowinda zace zonse
zidzakhazikika, ndi codziletsa ciri: conse wamanga naco moyo
wace cidzakhazikika. 5Koma atate wace akamletsa tsiku lakumva
iye; zowinda zace zonse, ndi zodziletsa zace zonse anamanga nazo
moyo wace, sizidzakhazikika; ndipo Yehova adzamkhululukira,
popeza atate wace anamletsa. 6Ndipo akakwatibwa naye
mwamuna, pokhala ali nazo zowinda zace, kapena zonena
zopanda pace za milomo yace, zimene anamanga nazo moyo
wace; 7nakazimva mwamuna wace, nakakhala naye cete tsiku
lakuzimva iye; pamenepo zowinda zace zidzakhazikika, ndi
zodziletsa anamanga nazo moyo wace zidzakhazikika. 8Kama
mwamuna wace akamletsa tsiku lakumva iye; pamenepo
adzafafaniza cowinda cace anali naco, ndi zonena zopanda pace za
milomo yace, zimene anamanga nazo moyo wace; ndipo Yehova
adzamkhululukira. 9Koma cowinda ca mkazi wamasiye, kapena
mkazi wocotsedwa, ziti zonse anamanga nazo moyo wace
zidzamkhazikikira. 10Ndipo ngati anawinda m'nyumba ya
mwamuna wace, kapena anamanga moyo wace ndi codziletsa ndi
kulumbirapo, 11ndipo mwanuna wace anamva, koma anakhala
naye cete osamletsa, pamenepo zowinda zace zonse
zidzakhazikika, ndi zodziletsa zonse anamanga nazo moyo wace
zidzakhazikika. 12Koma ngati mwamuna wace anazifafanizadi tsiku
lakuzimva iye, zonse zoturuka m'milomo yace kunena za zowinda
zace, kapena za codziletsa ca moyo wace sizidzakhazikika;
mwamuna wace anazifafaniza; ndipo Yehova adzamkhululukira
Iye. 13Cowinda ciri conse, ndi columbira ciri conse codziletsa
cakucepetsa naco moyo, mwamuna wace acikhazikira, kapena
mwamuna wace acifafaniza. 14Koma mwamuna wace akakhala
naye cete tsiku ndi tsiku; pamenepo akhazikira zowinda zace
zonse, kapena zodziletsa zace zonse, ziri pa iye; wazikhazikitsa,
popeza anakhala naye cete tsikuli anazimva iye. 15Koma
akazifafaniza atatha kuzimva; pamenepo adzasenza mphulupulu
yace. 16Awa ndi malemba amene Yehova analamulira Mose, a

pakati pa mwamuna ndi mkazi wace, pakati pa atate ndi mwana wace wamkazi, akali namwali, m'nyumba ya atate wace.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Aisrayeli agonjetsa Amidyani

1Ndipo Yehova ananena ndi Mose, nati, 2Abwezereni cilango
Amidyani cifukwa ca ana a Israyeli; utatero udzaitanidwa kumka
kwa anthu a mtundu wako. 3Ndipo Mose ananena ndi anthu, nati,
Adzikonzere ena mwa inu zida za nkhondo, alimbane nao
Amidyani, kuwabwezera Amidyani cilango ca Yehova. 4Muwatume
kunkhondo a pfuko limodzi, cikwi cimodzi, a pfuko limodzi cikwi
cimodzi, atere mafuko onse a Israyeli. 5Ndipo anapereka mwa zikwi
za Israyeli, a pfuko limodzi cikwi cimodzi, anthu zikwi khumi ndi
ziwiri okonzekeratu ndi zankhondo. 6Ndipo Mose anawatuma a
pfuko limodzi cikwi cimodzi, kunkhondo, iwowa ndi Pinehasi
mwana wa Eleazara wansembe, kunkhondo, ndi zipangizo
zopatulika, ndi malipenga oliza m'dzanja lace. 7Ndipo anawathira
nkhondo Amidyani, monga Yehova adamuuza Mose; nawapha
amuna onse. 8Ndipo anapha mafumu a Amidyani pamodzi ndi
ophedwa ao ena; ndiwo Evi, ndi Rekamu, ndi Zuri, ndi Huri, ndi
Reba, mafumu asanu a Amidyani; namupha Balamu mwana wa
Beori ndi lupanga. 9Ndipo ana a Israyeli anagwira akazi a
Amidyani, ndi ana ang'ono, nafunkha ng'ombe zao zonse, ndi
zoweta zao zonse, ndi cuma cao conse. 10Ndipo anatentha ndi
moto midzi yao yonse yokhalamo iwo, ndi zigono zao
zonse. 11Ndipo anapita nazo zofunkha zonse, ndi zakunkhondo
zonse, ndizo anthu ndi nyama. 12Ndipo anadza nao andende, ndi
zakunkhondo, ndi zofunkha, kwa Mose, ndi kwa Eleazara
wansembe, ndi kwa khamu la ana a Israyeli, kucigono, ku zidikha
za Moabu, ziri ku Yordano pafupi pa Yeriko.

Mayeretsedwe a ankhondowo

13Ndipo Mose, ndi Eleazara wansembe, ndi akalonga onse a
khamulo, anaturuka kukomana nao kunja kwa cigono. 14Ndipo
Mose anakwiya nao akazembe a nkhondoyi, atsogoleri a zikwi,
atsogoleri a mazana, akufuma kunkhondo adaithira. 15Ndipo Mose
ananena nao, Kodi mwasunga ndi moyo akazi onse? 16Taonani,
awa analakwitsa ana a Israyeli pa Yehova nilica Peoricija, monga
adawapangira Balamu; kotero kuti kunali mliri m'khamu la
Yehova. 17Ndipo tsono iphani amuna onse mwa anawo, iphaninso
akazi onse akudziwa mwamuna mogona naye. 18Koma ana akazi
onse osadziwa mwamuna mogona naye, asungeru ndi moyo
akhale anu. 19Ndipo mukhale m'misasa kunja kwa cigono masiku
asanu ndi awiri; ali yense adapha munthu, ndi ali yense
wakukhudza wophedwa, mudziyeretse tsiku lacitatu ndi lacisanu
ndi ciwiri, inu ndi andende anu. 20Muyeretse zobvala zanu zonse,
zipangizo zonse zacikopa, ndi zaomba zonse za ubweya wa mbuzi,
ndi zipangizo zonse zamtengo. 21Ndipo Eleazara wansembe

ananena ndi ankhondo adapita kunkhondowo, Lemba la cilamuloco
Yehova analamulira Mose ndi ili: 22Golidi, ndi siliva, mkuwa, citsulo,
ndolo ndi mtobvu zokha, 23zonse zakulola moto, mupititse m'moto,
ndipo zidzakhala zoyera; koma muziyeretsenso ndi madzi
akusiyanitsa. Koma zonse zosalola moto, muzipititse
m'madzi. 24Ndipo muzitsuke zobvala zanu tsiku lacisanu ndi ciwiri,
kuti mukhale oyera; ndipo mutatero mulowe m'cigono.

Magawidwe a zofunkha

25Ndipo Yehova ananena ndi Mose, nati, 26Werengani
zakunkhondo, ndizo anthu, ndi zoweta, iwe; ndi Eleazara
wansembe, ndi akuru a nyumba za makolo za khamulo; 27nugawe
zakunkhondo pawiri; pakati pa othira nkhondo amene anaturuka
kunkhondo, ndi khamu lonse. 28Ndipo usonkhetse anthu ankhondo
akuturuka kunkhondo apereke kwa Yehova; munthu mmodzi mwa
anthu mazana asanu, mwa ng'ombe, mwa aburu, mwa nkhosa ndi
mbuzi, momwemo. 29Uzitenge ku gawo lao, ndi kuzipereka kwa
Eleazara wansembe, zikhale nsembe yokweza ya Yehova. 30Ndipo
ku gawo la ana a Israyeli utenge munthu mmodzi mwa anthu
makumi asanu, mwa ng'ombe, mwa aburu, mwa nkhosa ndi mbuzi,
mwa zoweta zonse, momwemo; nuzipereke kwa Alevi, akusunga
udikiro wa kacisi wa Yehova. 31Ndipo Mose ndi Eleazara wansembe
anacita monga Yehova anamuuza Mose. 32Ndipo zakunkhondo,
zotsalira zofunkha zonse adazifunkha ankhondowa, ndizo nkhosa
zikwi mazana asanu ndi limodzi mphambu zikwi makumi asanu ndi
awiri kudza zisanu, 33ndi ng'ombe zikwi makumi asanu ndi awiri
mphambu ziwiri, 34ndi aburu zikwi makumi asanu ndi limodzi
mphambu cimodzi, 35ndi anthu, ndiwo akazi osadziwa mwamuna
mogona naye, onse pamodzi zikwi makumi atatu ndi ziwiri. 36Ndipo
limodzi la magawo awiri, ndilo gawo la iwo adaturuka kunkhondo,
linafikira nkhosa zikwi mazana atatu mphambu makumi atatu
kudza zisanu ndi ziwiri mphambu mazana asanu. 37Ndi msonkho
wa Yehova wankhosa ndiwo mazana asanu ndi limodzi mphambu
makumi asanu ndi awiri mphambu zisanu. 38Ndipo ng'ombe
zidafikira zikwi makumi atatu mphambu zisanu ndi cimodzi;
pamenepo msonkho wa Yehova ndiwo makumi asanu ndi awiri
mphambu ziwiri. 39Ndipo aburu anafikira zikwi makumi atatu ndi
mazana asanu; pamenepo msonkho wa Yehova ndiwo makumi
asanu ndi limodzi mphambu mmodzi. 40Ndipo anthu anafikira zikwi
khumi ndi zisanu ndi cimodzi; pamenepo msonkho wa Yehova
ndiwo anthu makumi atatu mphambu awiri. 41Ndipo Mose
anapereka zamsonkhozo, ndizo nsembe yokweza ya Yehova, kwa
Eleazara wansembe, monga Yehova adamuuza Mose. 42Ndipo
kunena za gawo la ana a Israyeli, limene Mose adalicotsa kwa
anthu ocita nkhondowo, 43(ndipo gawo la khamulo ndilo nkhosa

zikwi mazana atatu mphambu makumi atatu kudza zisanu ndi ziwiri mphambu mazana asanu, 44ndi ng'ombe zikwi makumi atatu mphambu zisanu ndi cimodzi, 45ndi aburu zikwi makumi atatu ndi mazana asanu, 46ndi anthu zikwi khumi ndi zisanu ndi cimodzi,) 47mwa gawolo la ana a Israyeli Mose anatenga munthu mmodzi mwa makumi asanu, ndi zoweta momwemo, nazipereka kwa Alevi, akusunga udikiro wa kacisi wa Yehova; monga Yehova adamuuza Mose.

Zopereka zaufulu za akazembe

48Pamenepo akazembe a pa ankhondo zikwi, atsogoleri a zikwi, ndi atsogoleri a mazana, anayandikiza kwa Mose; 49nati kwa Mose, Atumiki anu anawerenga ankhondo tinali nao, ndipo sanasowa munthu mmodzi wa ife. 50Ndipo tabwera naco copereka ca Yehova, yense cimene anacipeza, zokometsera zagolidi, unyolo, zikwinjiri, mphete zosindikizira, nsapule, ndi mkanda, kucita cotetezera moyo wathu pamaso pa Yehova. 51Ndipo Mose ndi Eleazara wansembe analandira golidiyo kwa iwowo, ndizo zokometsera zonse zokonzeka. 52Ndipo golidi yense wa nsembe yokweza ya Yehova amene anapereka kwa Yehova, wofuma kwa atsogoleri a zikwi, ndi atsogoleri a mazana, ndiwo masekeli zikwi khumi ndi zisanu ndi cimodzi mphambu mazana asanu ndi awiri kudza makumi asanu. 53Popeza wankhondo yense anadzifunkhira yekha. 54Ndipo Mose ndi Eleazara wansembe analandira golidi kwa akuru a zikwi ndi a mazana, nalowa naye ku cihema cokomanako, cikumbutso ca ana a Israyeli pamaso pa Yehova.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Arubeni, Agadi, ndi Amanase alandira colowa cao tsidya lino la Yordano

1Koma ana a Rubeni ndi ana a Gadi anali nazo zoweta
zambirimbiri; ndipo anapenyerera dziko la Yazeri, ndi dziko la
Gileadi, ndipo taonani, malowo ndiwo malo a zoweta. 2Pamenepo
ana a Gadi ndi ana a Rubeni anadza nanena ndi Mose, ndi Eleazara
wansembe, ndi akalonga a khamulo, nati, 3Ataroti, ndi Diboni, ndi
Yazeri, ndi Nimra, ndi Heseboni, ndi Eleyali, ndi Sebamu, ndi Nebo,
ndi Beoni, 4dzikoli Yehova analikantha pamaso pa khamu la
Israyeli, ndilo dziko la zoweta ndipo anyamata anu ali nazo
zoweta. 5Ndipo anati, Ngati tapeza ufulu pamaso panu, mupatse
anyamata anu dziko ili likhale lao lao; tisaoloke Yordano. 6Ndipo
Mose anati kwa ana a Gadi ndi ana a Rubeni, Kodi abale anu apite
kunkhondo, ndi inu mukhale pansi kuno? 7Ndipo mufoketseranji
mtima wa ana a Israyeli kuti asaoloke ndi kulowa dzikoli Yehova
anawapatsa? 8Anatero makolo anu, muja ndinawatumiza acoke ku
Kadesi Barinea kukaona dziko. 9Popeza atakwera kumka ku cigwa
ca Esikolo, naona dziko, anafoketsa mtima wa ana a Israyeli, kuti
asalowe dzikoli Yehova adawapatsa. 10Ndipo Yehova anapsa mtima
tsiku lija, nalumbira iye, nati, 11Anthu adakwerawo kuturuka
m'Aigupto, kuyambira wa zaka makumi awiri ndi mphambu
sadzaona dziko limene ndinalumbirira Abrahamu, ndi Isake, ndi
Yakobo; popeza sananditsata Ine ndi mtima wonse; 12koma Kalebi
mwana wa Yefune, Mkenizi, ndi Yoswa mwana wa Nuni ndiwo;
popeza anatsata Yehova ndi mtima wonse. 13Ndipo Yehova anapsa
mtima pa Israyeli, nawayendetsa-yendetsa m'cipululu zaka
makumi anai, kufikira utatha mbadwo wonsewo udacita coipa
pamaso pa Yehova. 14Ndipo taonani, mwauka m'malo mwa makolo
anu, gulu la anthu ocimwa, kuonjezanso mkwiyo waukali wa
Yehova pa Israyeli, 15Pakuti mukabwerera m'mbuyo kusamtsata
iye, adzawasiyanso m'cipululu, ndipo mudzaononga anthu awa
onse. 16Ndipo anayandikiza, nati, Tidzamangira zoweta zathu
makola kuno, ndi ana athu midzi; koma ife tidzakhala okonzeka ndi
kufulumira pamaso pa ana a Israyeli, kufikira tidawafikitsa kumalo
kwao; 17ndi ang'ono athu adzakhala m'midzi ya malinga cifukwa ca
okhala m'dzikomo. 18Sitidzabwerera kwathu, kufikira ana a Israyeli
atalandira yense colowa cace. 19Pakuti sitidzalandira pamodzi nao
tsidya la Yordano, ndi m'tsogolo mwace; popeza colowa cathu
tacilandira tsidya lino la Yordano kum'mawa. 20Ndipo Mose anati
nao, Ngati mudzacita ici, ndi kudzikonza kunkhondo pamaso pa
Yehova, 21ndi kuoloka Yordano pamaso pa Yehova okonzeka onse
mwa inu, kufikira atapitikitsa adani ace pamaso pace, 22ndi dziko
lagonjera Yehova; mutatero mudzabwerere, ndi kukhala

osacimwira Yehova ndi Israyeli; ndipo dziko ili lidzakhala lanu lanu pamaso pa Yehova. 23Koma mukapanda kutero, taonani, mwacimwira Yehova; ndipo zindikirani kuti cimo lanu lidzakupezani. 24Dzimangireni midzi ya ana anu, ndi makola a zoweta zanu; ndipo muzicite zoturuka m'kamwa mwanu.
25Ndipo ana a Gadi ndi ana a Rubeni ananena ndi Mose, nati, Anyamata anu adzacita monga mbuyanga alamulira. 26Ana athu, akazi athu, zoweta zathu, ndi ng'ombe zathu zonse, zidzakhala komweko m'midzi ya ku Gileadi; 27koma anyamata anu adzaoloka, yense wokonzekera ndi zankhondo pamaso pa Yehova kunkhondo, monga wanena mbuyanga.
28Pamenepo Mose anamuuza Eleazara wansembe, ndi Yoswa mwana wa Nuni, ndi akuru a makolo a mapfuko a ana a Israyeli za iwo. 29Ndipo Mose anati kwa iwo, Ngati ana a Gadi ndi ana a Rubeni aoloka nanu Yordano, yense wokonzekera ndi zankhondo pamaso pa Yehova, ndi dziko lagonjera inu; pamenepo muwapatse dziko la Gileadi likhale lao lao; 30koma akapanda kuoloka nanu okonzeka, akhale nao maiko ao ao pakati pa inu m'dziko la Kanani. 31Ndipo ana a Gadi ndi ana a Rubeni anayankha, nati, Monga Yehova anati kwa anyamata anu momwemo tidzacita. 32Tidzaoloka okonzeka pamaso pa Yehova ku dziko la Kanani, koma colowa cathu cathu cikhale tsidya lino la Yordano. 33Ndipo Mose anawapatsa, ndiwo ana a Gadi, ndi ana a Rubeni ndi pfuko la hafu la Manase mwana wa Yosefe, dziko la Sihoni mfumu ya Aamori, ndi dziko la Ogi mfumu ya Basana, dzikoli ndi midzi yace m'malire mwao, ndiyo midzi ya dziko lozungulirako, 34Ndipo ana a Gadi anamanga Diboni, ndi Ataroti, ndi Aroeri; 35Ataroti Sofani, Yazeri, ndi Yogebeha; 36ndi Beti Nimira, ndi Beti Harani: midzi ya m'malinga, ndi makola a zoweta. 37Ndipo ana a Rubeni anamanga Hesiboni, ndi Eleyali, ndi Kiriyataimu; 38ndi Nebo, ndi Baala Meoni (nasintha maina ao), ndi Sibima; ndipo anaicha midzi adaimanga ndi maina ena. 39Ndipo ana a Makiri mwana wa Manase anamka ku Gileadi, naulanda, napitikitsa Aamori anali m'mwemo. 40Ndipo Mose anapatsa Makiri mwana wa Manase Gileadi; ndipo anakhala m'menemo. 41Ndipo Yairi mwana wa Manase anamka nalanda midzi yao, naicha Havoti Yairi. Ndipo Noba anamka nalanda Kenati, ndi miraga yace, naucha Noba, dzina lace.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Za ulendo wa Aisrayeli pakati pa Ramese ndi Sitimu

1Maulendo a ana a Israyeli amene anaturuka m'dziko la Aigupto
monga mwa makamu ao, ndi dzanja la Mose ndi Aroni, ndi
awa. 2Ndipo Mose analembera maturukidwe ao monga mwa
maulendo ao, monga mwa mau a Yehova; ndipo maulendo ao ndi
awa monga mwa maturukidwe ao. 3Ndipo anacokera ku Ramese
mwezi woyamba, tsiku lakhumi ndi cisanu la mwezi woyamba;
atacita Paskha m'mawa mwace ana a Israyeli, anaturuka ndi
dzanja lokwezeka pamaso pa Aaigupto onse, 4pamene Aaigupto
ailalikuika oyamba kubadwa ao onse, amene Yehova adawakantha;
Yehova adaweruzanso milungu yao. 5Ndipo ana a Israyeli
macokera ku Ramese, nayenda namanga ku Sukoti. 6Nacokera ku
Sukoti, nayenda namanga m'Etamu, ndiko ku malekezero a
cipululu. 7Ndipo anacokera ku Etamu, nayenda nabwerera ku
Pihahiroti, ndiko kutsogolo kwace kwa Baala Zefoni; namanga iwo
patsogolo pa Migidoli. 8Ndipo anacokera ku Pihahiroti, naoloka
pakati pa nyanja nalowa m'cipululu; nayenda ulendo wa masiku
atatu m'cipululu ca Etamu, namanga m'Mara. 9Ndipo anacokera ku
Mara, nayenda nafika ku Elimu, ku Elimu ndiko kuli akasupe khumi
ndi awiri a madzi, ndi akanjedza makumi asanu ndi awiri; namanga
iwo komweko. 10Ndipo anacokera ku Elimu, nayenda namanga ku
Nyanja Yofiira. 11Nacokera ku Nyanja Yofiira, nayenda namanga
m'cipululu ca Sini. 12Nacokera ku cipululu ca Sini, nayenda
namanga m'Dofika. 13Nacokera ku Dofika, nayenda namanga
m'Alusi. 14Nacokera ku Alusi, nayenda namanga m'Refidimu;
kumeneko kunalibe madzi kuti anthu amwe. 15Ndipo anacokera ku
Refidimu, nayenda namanga m'cipululu ca Sinai. 16Nacokera ku
cipululu ca Sinai, nayenda namanga m'Kibiroti Hatava. 17Nacokera
ku Kibiroti Hatava, nayenda namanga m'Hazeroti. 18Nacokera ku
Hazeroti, nayenda namanga m'Ritima. 19Nacokera ku Ritima,
nayenda namanga m'Rimoni Perezi. 20Nacokera ku Rimoni Perezi,
nayenda namanga m'Libina. 21Nacokera ku Libina, nayenda
namanga m'Risa. 22Nacokera ku Risa, nayenda namanga
m'Kehelata. 23Nacokera ku Kehelata, nayenda namanga m'phiri la
Saferi. 24Nacokera ku phiri la Saferi, nayenda namanga
n'Harada. 25Nacokera ku Harada, nayenda namanga
m'Makeloti. 26Nacokera ku Makeloti, nayenda namanga
m'Tahata. 27Nacokera ku Tahata, nayenda namanga
m'Tara. 28Nacokera ku Tara, nayenda namanga
m'Mitika. 29Nacokera ku Mitika, nayenda namanga
m'Hasimona. 30Nacokera ku Hasimona, nayenda namanga
m'Moseroto. 31Nacokera ku Moseroto, nayenda namanga m'Bene
Yaakana. 32Nacokera ku Bene Yaakana, nayenda namanga m'Hori

Hagidigadi. 33Nacokera ku Hori Hagidigadi, nayenda namanga
m'Yotibata. 34Nacokera ku Yotibata, nayenda namanga
m'Abirona. 35Nacokera ku Abirona, nayenda namanga m'Ezioni
Geberi. 36Nacokera ku Ezioni Geberi, nayenda namanga m'cipululu
ca Zini (ndiko Kadesi). 37Nacokera ku Kadesi, nayenda namanga
m'phiri la Hori, ku malekezero a dziko la Edomu. 38Ndipo Aroni
wansembe anakwera m'phiri la Hori pa mau a Yehova, nafa
komweko, ataturuka ana a Israyeli m'dziko la Aigupto zaka makumi
anai, mwezi wacisanu, tsiku loyamba la mwezi. 39Ndipo Aroni ndiye
wa zaka zana limodzi mphambu makumi awiri kudza zitatu pakufa
iye m'phiri la Hori. 40Ndipo Mkanani, mfumu ya Aradi, wakukhala
kumwela m'dziko la Kanani, anamva za kudza kwao kwa ana a
Israyeli. 41Ndipo anacokera ku phiri la Hori, nayenda namanga
m'Tsalimona. 42Nacokera ku Tsalimona, nayenda namanga
m'Punoni. 43Nacokera ku Punoni, nayenda namanga
m'Oboti. 44Nacokera ku Oboti, nayenda namanga m'iye Abarimu,
m'malire a Moabu. 45Nacokera ku Iyimu, nayenda namanga
m'Diboni Gadi. 46Nacokera ku Diboni Gadi, nayenda namanga
m'Alimoni Diblataimu. 47Nacokera ku Alimoni Diblataimu, nayenda
namanga m'mapiri a Abarimu, cakuno ca Nebo. 48Nacokera ku
mapiri a Abarimu, nayenda namanga m'zidikhaza Moabu pa
Yordano ku Yeriko, 49Ndipo anamanga pa Yordano, kuyambira ku
Beti Yesimoti kufikira ku Abeli Sitimu m'zidikha za Moabu.

Aisrayeli azipitikitsa eni dziko la Kanani

50Ndipo Yehova ananena ndi Mose m'zidikha za Moabu pa
YordaBaku Yeriko, nati, 51Nena ndi ana a Israyeli, nuti nao,
Mutaoloka Yordano kulowa m'dziko la Kanani, 52mupitikitse onse
okhala m'dzikopamaso panu, ndi kuononga mafano ao onse a
miyala, ndi kuononga mafano ao onse oyenga, ndi kupasula
misanje yao yonse; 53ndipo mulande dziko, ndi kukhala m'mwemo,
pakuti ndinakupatsani inu dzikoli likhale lanu lanu. 54Ndipo
mulandire dzikoli ndi kucita maere monga mwa mabanja anu;
colowa cao cicurukire ocurukawo, colowa cao cicepere ocepawo;
kumene maere amgwera munthu, kumeneko nkwace; mulandire
colowa canu monga mwa mapfuko a makolo anu. 55Koma
mukapanda kupitikitsa okhala m'dziko pamaso panu, pamenepo
iwo amene muwalola atsale adzakhala ngati zotwikira m'maso
mwanu, ndi minga m'mbali zanu, nadzakubvutani m'dziko limene
mukhalamo. 56Ndipo kudzakhala kuti monga ndinayesa kucitira
iwowa, ndidzakucitirani inu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Malire a dziko la Kanani

1Ndipo Yehova ananena ndi Mose, nati, 2Uza ana Israyeli, nunene
nao, Mutalowa a m'dziko la Kanani, ndilo dziko logwera inu, likhale
colowa canu, dziko ija Kanani monga mwa malire ace, 3dera lanu la
kumwela lidzakhala locokera ku cipululu ca Zini, kutsata
m'mphepete mwa Edomu, ndi malire anu a kumwela adzakhala
ocokera ku malekezero a Nyanja ya Mcere kum'mawa; 4ndi malire
anu adzapinda kucokera kumwela kumka pokwera Akrabimu, ndi
kupitirira ku Zini; ndi kuturuka kwace adzacokera kumwela ku
Kadesi Barinea, nadzaturuka kumka ku Hazara Adara, ndi kupita
kumka ku Azimoni; 5ndipo malirewo adzapinda ku Azimoni kumka
ku mtsinje wa Aigupto, ndi kuturuka kwao adzaturuka
kunyanja. 6Kunena za malire a kumadzulo, nyanja yaikuru ndiyo
malire anu; ndiyo malire anu a kumadzulo. 7Malire anu a kumpoto
ndiwo: kuyambira ku nyanja yaikuru mulinge ku phiri la
Hori: 8kucokera ku phiri la Hori mulinge polowera Hamati; ndipo
kuturuka kwace kwa malire kudzakhala ku Zedadi. 9Ndipo
malirewo adzaturuka kumka ku Zifironi, ndi kuturuka kwace
kudzakhala ku Hazara Enani; ndiwo malire anu a kumpoto. 10Ndipo
mudzilembere malire a kum'mawa ocokera ku Hazara Enani kumka
ku Sefamu; 11ndi malire adzatsika ku Sefamu kumka ku Ribala,
kum'mawa kwa Ayina; ndipo malire adzatsika, nadzafikira mbali ya
nyanja ya Kinereti kum'mawa, 12ndi malire adzatsika ku Yordano,
ndi kuturuka kwace kudzakhala ku Nyanja ya Mcere; ili ndili dziko
lanu monga mwa malire ace polizinga. 13Ndipo Mose anauza ana a
Israyeli, nati, Ili ndi dzikoli mudzalandira ndi kucita maere, limene
Yehova analamulira awapatse mapfuko asanu ndi anai ndi
hafu; 14popeza pfuko la ana a Rubeni monga mwa nyumba za
makolo ao, ndi pfuko la ana a Gadi monga mwa nyumba za makolo
ao, adalandira, ndi pfuko la hafu la Manase lalandira colowa
cao; 15mapfuko awiriwa ndi hafu adalandira colowa cao tsidya lija
la Yordano ku Yeriko, kum'mawa, koturukira dzuwa.
16Ndipo Yehova ananena ndi Mose, nati, 17Maina a amunawo
adzakugawirani dziko likhale colowa canu, ndi awa: Eleazara
wansembe, ndi Yoswa mwana wa Nuni. 18Muwatengenso akalonga,
kalonga mmodzi ku pfuko limodzi, agawe dziko likhale colowa
cao. 19Maina a amunawo ndiwo: wa pfuko la Yuda, Kalebi mwana
wa Yefune. 20Wa pfuko la ana a Simeoni, Semuyeli mwana wa
Amihudi. 21Wa pfuko la Benjamini, Elidadi mwana wa Kisiloni. 22Wa
pfuko la ana a Dani, kalonga Buki mwana wa Yogili. 23Wa ana a
Yosefe; wa pfuko la ana a Manase, kalonga Haniyeli mwana wa
Efodi. 24Wa pfuko la ana a Efraimu, kalonga Kemuyeli mwana wa
Sipitana. 25Wa pfuko la ana a Zebuloni, kalonga Elisafana mwana

wa Paranaki. 26Wa pfuko la ana a Isakara, kalonga Palitiyeli mwana
wa Azana. 27Wa pfuko la ana a Aseri, kalonga Ahihudi mwana wa
Selomi. 28Wa pfuko la ana a Nafitali, kalonga Pedaheli mwana wa
Amihudi. 29Iwo ndiwo amene Yehova analamulira agawire ana a
Israyeli colowa cao m'dziko la Kanani.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Midzi ya Alevi

1Ndipo Yehova ananena ndi Mose m'zidikha za Moabu, pa Yordano,
ku Yeriko, ndi kuti, 2Uza ana a Israyeli, kuti apatseko Alevi colowa
cao cao, midzi yokhalamo; muwapatsenso Alevi mabusa
akuzungulira midzi. 3Ndipo midzi ndiyo yokhalamo iwowa; ndi
mabusa akhale a ng'ombe zao, ndi zoweta zao, inde nyama zao
zonse. 4Ndipo mabusa a midziyo, imene muipereke kwa Alevi
ndiwo a mikono cikwi cimodzi kuyambira kulinga kufikira
kunja. 5Ndipo muyese kunja kwa mudzi, mbali ya kum'mawa
mikono zikwi ziwiri, ndi mbali ya kumwela mikono zikwi ziwiri, ndi
mbali ya kumadzulo mikono zikwi ziwiri, ndi mbali ya kumpoto
mikono zikwi ziwiri; ndi mudziwo pakati; ndiwo mabusa a
kumidzi. 6Ndipo midziyo muipereke kwa Alevi ndiyd midzi ija isanu
ndi umodzi yopulumukirako; imene muipereke kuti wakupha
mnzace athawireko; ndipo pamodzi ndi iyi muperekenso midzi
makumi anai ndi iwiri. 7Midzi yonse muipereke kwa Alevi ndiyo
midzi makumi anai ndi isanu ndi itatu, iyo pamodzi ndi mabusa
ao. 8Ndipo kunena za midziyo muiperekeyo yao yao ya ana a
Israyeli, okhala nayo yambiri mutengeko yambiri; okhala nayo
pang'ono mutengeko pang'ono; onse operekako midzi yao kwa
Alevi monga mwa colowa cao adacilandira.

Midzi yopulumukirako

9Ndipo Yehova ananena ndi Mose, nati, 10Nenandi ana a Israyeli,
nuti nao, Pakuoloka inu Yordano kulowa m'dziko la
Kanani, 11muikire midzi ikukhalireni midzi yopulumukirako; kuti
wakupha mnzace wosati dala athawireko. 12Ndipo midziyo
ikukhalireni yakupulumuka wolipsa; kuti wakupha mnzace asafe,
kufikira ataima pamaso pa msonkhano amweruze. 13Ndipo midziyo
muipereke ikukhalireni midzi isanu ndi umodzi
yopulumukirako. 14Mupereke midzi itatu tsidya lino la Yordano, ndi
midzi itatu mupereke m'dziko la Kanani, ndiyo
yopulumukirako. 15Midzi isanu ndi umodzi imene ndiyo
yopulumukirako ana a Israyeli, ndi mlendo, ndi wokhala pakati pao;
kuti ali yense adamupha munthu osati dala athawireko. 16Koma
akamkantha ndi cipangizo cacitsulo, kuti wafa, ndiye wakupha
munthu; wakupha munthu nayenso amuphe ndithu. 17Kapena
akamkantha m'dzanja muli mwala, wakufetsa munthu, ndipo wafa,
ndiye wakupha munthu; wakupha munthu nayenso amuphe
ndithu. 18Kapena akamkantha m'dzanja muli cipangizo camtengo,
cakufetsa munthu, ndipo wafa, ndiye wakupha munthu; wakupha
munthu nayenso amuphe ndithu. 19Wolipsa mwazi mwini wace
aphe wakupha munthuyo; pakumkumika amuphe, 20Ndipo
akampyoza momkwiyira, kapena kumponyera kanthu momlalira,

kuti wafa; 21kapena kumpanda ndi dzanja lace momuda, kuti wafa, womkanthayo nayenso amuphe ndithu; ndiye wakupha munthu; wolipsa mwazi aphe wakupha munthuyo pomkumika. 22Koma akampyoza modzidzimuka, osamuda, kapena kumponyera kanthu osamialira, 23kapena kumponyera mwala wakufetsa munthu, osamuona, namgwetsera uwu, kuti wafa, koma sindiye mdani wace, kapena womfunira coipa; 24pamenepo msonkhano uziweruza pakati pa wokantha mnzaceyo ndi wolipsa mwaziyo monga mwa maweruzo awa; 25ndipo msonkhano umlanditse wakupha munthu m'dzanja la wolipsa mwazi, ndi msonkhanowo umbwezere ku mudzi wace wopulumukirako, kumene adathawirako; ndipo azikhalamo kufikira atafa mkulu wa ansembe wodzozedwa ndi mafuta opatulika. 26Koma wakupha munthu akaturuka nthawi iri yonse kulumpha malire a mudzi wace wopulumukirako kumene anathawirako; 27nakampeza wolipsa mwazi kunja kwa malire a mudzi wace wothawirako, ndipo wolipsa mwazi akapha wakupha munthu, alibe kucimwira mwazi; 28popeza wakupha munthu akadakhala m'mudzi wace wopulumukirako kufikira atafa mkulu wa ansembe; koma atafa mkulu wa ansembe wakupha munthuyo abwere ku dziko lace lace. 29Ndipo izi zikhale kwa inu lemba la ciweruzo mwa mibadwo yanu, m'nyumba zanu zonse. 30Ali yense wakantha munthu, wakupha munthuyo aziphedwa pakamwa pa mboni; koma mboni ya munthu mmodzi isafikire kuti munthu afe. 31Musamalandira dipo lakuombola moyo wa iye adapha munthu, naparamula imfa; koma aziphedwa ndithu. 32Musamalandira dipo lakuombola iye amene adathawira ku mudzi wace wopulumukirako, kuti abwerenso kukhala m'dziko, kufikira atafa wansembe. 33Ndipo musamaipsa dziko muli m'mwemo; popeza mwazi uipsa dziko; pakuti kulibe kutetezera dziko cifukwa ca mwazi anaukhetsa m'mwemo, koma ndi mwazi wa iye anaukhetsa ndiwo. 34Usamadetsa dziko ukhala m'mwemo, limene ndikhalitsa pakati pace; popeza Ine Yehova ndikhalitsa pakati pa ana a Israyeli.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Za kukwatibwa kwa ana akazi olandira colowa

1Ndipo akuru a makolo a mabanja a ana a Gileadi, mwana wa
Makiri, mwana wa Manase, wa mabanja a ana a Yosefe,
anayandikiza, nanena pamaso pa Mose, ndi pamaso pa akalonga,
ndiwo akuru a makolo a ana a Israyeli; 2nati, Yehova analamulira
mbuye wanga mupatse ana a Israyeli dzikoli mocita maere likhale
colowa cao; ndipo Yehova analamulira mbuye wathu mupatse ana
ace akazi colowa ca Tselofekadi mbale wathu. 3Ndipo akakwatibwa
nao ana amuna a mapfuko ena a ana a Israyeli, acicotse colowa
cao ku colowa ca makolo athu, nacionjeze ku colowa ca pfuko
limene adzakhalako; cotero acicotse ku maere a colowa
cathu. 4Ndipo pofika caka coliza ca ana a Israyeli adzaphatikiza
colowa cao ku colowa ca pfuko limene akhalako; cotero adzacotsa
colowa cao ku colowa ca pfuko la makolo athu. 5Ndipo Mose
analamulira ana a Israyeli monga mwa mau a Yehova, nati, Pfuko
la ana a Yosefe linena zaona. 6Colamulira Yehova za ana akazi a
Tselofekadi ndi ici, kuti, Akwatibwe nao amene afuna eni ace;
komatu akwatibwe nao a banja la pfuko la makolo ao okha
okha. 7Motero colowa ca ana a Israyeli sicidzamka m'pfuko
m'pfuko; popeza ana a Israyeli adzamamatira yense ku colowa ca
pfuko la makolo ace. 8Ndipo mwana wamkazi yense wa mapfuko a
ana a Israyeli, wakukhala naco colowa, akwatibwe ndi wina wa
banja la pfuko la kholo lace, kuti ana a Israyeli akhale naco yense
colowa ca makolo ace. 9Motero colowa ca ana a Israyeli sicidzamka
m'pfuko m'pfuko, pakuti mapfuko a ana a Israyeli adzamamatira
lonse ku colowa cace cace. 10Monga Yehova adalamulira Mose,
momwemo ana akazi a Tselofekadi anacita; 11popeza Mala, Tiriza,
ndi Hogila, ndi Milika, ndi Nowa, ana akazi a Tselofekadi,
anakwatibwa ndi ana amuna a abale a atate wao. 12Anakwatibwa
mwa mabanja a ana a Manase mwana wa Yosefe; ndipo colowa cao
dnakhala m'pfuko la banja la atate wao.
13Awa ndi malamulo ndi maweruzo, amene Yehova analamulira
ana a Israyeli ndi dzanja la Mose m'zidikha za Moabu pa Yordano
ku Yeriko.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Deuteronomy

Deuteronomo 1

Mose awafotokozera za ulendo wao m'cipululu

1AWA ndi mau amene Mose ananena kwa Israyeli wonse, tsidya la Yordano
m'cipululu, m'cidikha ca pandunji pa Sufu, pakati pa Parani, ndi Tofeli, ndi
Labani, ndi Hazeroti, ndi Di Zahabi. 2Ulendo wace wocokera ku Horebe
wofikira ku Kadesi Barinea, wodzera njira ya phiri la Seiri, ndiwo wa masiku
khumi ndi limodzi. 3Ndipo kunali, caka ca makumi anai, mwezi wakhumi ndi
umodzi, tsiku loyamba la mweziwo, Mose ananena ndi ana a Israyeli, monga
mwa zonse Yehova adamlamulira awauze; 4atakantha Sihoni mfumu ya
Aamori, wakukhala m'Hesiboni, ndi Ogi mfumu ya Basana, wakukhala
m'Asitaroti, ku Edrei. 5Tsidya lija la Yordano, m'dziko la Moabu, Mose
anayamba kufotokozera cilamulo ici, ndi kuti. 6Yehova Mulungu wathu
ananena ndi ife m'Horebe, ndi kuti, Yakwanira nthawi yokhala inu m'phiri
muno; 7bwererani, yendani ulendo wanu ndi kumuka ku mapiri a Aamori, ndi
koyandikizana nao, kucidikha, kumapiri, ndi kunsi ndi kumwela, ndi
kumphepete kwa nyanja, dziko la Akanani, ndi Lebano, kufikira nyanja yaikuru
Firate. 8Taonani, ndakupatsani dzikoli pamaso panu, lowani landirani dziko
limene Yehova analumbirira makolo anu, Abrahamu, Isake, ndi Yakobo, kuti ili
ndidzawapatsa iwo ndi mbeu zao pambuyo pao. 9Ndipo muja ndinanena ndi
inu, ndi kuti, Sinditha ine kukunyamulani ndekha; 10Yehova Mulungu wanu
anakucurukitsani, ndipo taonani, lero mucuruka ngati nyenyezi za
kumwamba. 11Yehova Mulungu wa makolo anu, acurukitsire ciwerengero canu
calero ndi cikwi cimodzi, nakudalitseni monga iye ananena
nanu! 12Ndikasenza bwanji ndekha kupsinya kwanu, ndi katundu wanu, ndi
kulimbana kwanu? 13Dzifunireni amuna anzeru, ndi ozindikira bwino, ndi
odziwika mwa mafuko anu, ndipo ndidzawaika akhale akuru anu. 14Pamenepo
munandiyankha ndi kuti, Mau mwanenawa ndi abwino kuwacita. 15Potero
ndinatenga akuru a mapfuko anu, amuna anzeru, ndi odziwika, ndi kuwaika
akhale akuru anu, atsogoleri a zikwi, ndi atsogoleri a mazana, ndi atsogoleri a
makumi asanu, ndi atsogoleri a makumi, ndi akapitao, a mapfuko
anu. 16Ndipo ndinauza oweruza anu muja, ndi kuti, Mverani milandu ya pakati
pa abale anu, ndi kuweruza kolungama pakati pa munthu ndi mbale wace, ndi
mlendo wokhala naye. 17Musamasamalira munthu poweruza mlandu; ang'ono
ndi akuru muwamvere m'modzimodzi; musamaopa nkhope ya munthu;
popeza ciweruzo nca Mulungu; ndipo mlandu ukakulakani mubwere nao kwa
ine, ndidzaumva. 18Ndipo ndinakuuzani muja zonse muyenera kuzicita.
19Pamenepo tinayenda ulendo kucokera ku Horebe, ndi kubzyola m'cipululu
cacikuru ndi coopsa ciija conse munacionaci, pa njira ya ku mapiri a Aamori,
monga Yehova Mulungu wathu anatiuza; ndipo tinadza ku Kadesi
Barinea. 20Ndipo ndinati kwa inu, Mwafikira mapiri a Aamori, amene Yehova
Mulungu wathu atipatsa. 21Taonani, Yehova Mulungu wanu wapatsa dzikoli
pamaso panu; kwerakoni, landirani, monga Yehova Mulungu wa makolo anu,
wanena ndi inu; musamacita mantha, musamatenga nkhawa. 22Ndipo
munayandikiza kwa ine inu nonse, ndi kuti, Titumize amuna atitsogolere, kuti
akatizondere dziko ndi kutibwezera mau akunena za njira ya kukwera nayo ife
pomka komweko, ndi za midzi yoti tidzafikako. 23Ndipo cinandikomera cinthu
ici; ndipo ndinatenga amuna khumi ndi awiri ainu, pfuko limodzi mwamuna
mmodzi; 24amenewa anatembenuka nakwera kumapiri nalowa ku cigwa ca
Esikolo, nacizonda. 25Ndipo anatengako zipatso za dzikoli m'manja mwao,

natsikira nazo kwa ife, natibwezera mau ndi kuti, Dzikoli Yehova Mulungu wathu atipatsa ndi labwino. 26Koma simunafuna kukwerako, ndipo munapikisana nao mau a Yehova Mulungu wanu. 27Ndipo munadandaula m'mahema mwanu, ndi kuti, Popeza anatida Yehova, iye anatiturutsa m'dziko la Aigupto, kutipereka m'manja mwa Aamori, ationonge. 28Tikwere kuti? abale athu atimyukitsa mitima yathu, ndi kuti, Anthuwo ndiwo akulu ndi atali akuposa ife; midzi ndi yaikulu ndi ya malinga ofikira m'mwamba: tinaonakonso ana a Anaki. 29Pamenepo ndinati kwa inu, Musamaopsedwa, musamacita mantha nao. 30Yehova Mulungu wanu wakutsogolera inu, iye adzathirira inu nkhondo, monga mwa zonse anakucitirani m'Aigupto pamaso panu; 31ndi kucipululu, kumene munapenya kuti Yehova Mulungu wanu anakunyamulani, monga anyamula mwana wace wamwamuna, m'njira monse munayendamo, kufikira mutalowa m'malo muno. 32Koma m'cinthu ici simunakhulupirira Yehova Mulungu wanu, 33amene anakutsogolerani m'njira, kukufunirani malo akumanga mahema anu ndi mota usiku, kukuonetserani njira yoyendamo inu, ndi mumtambo usana. 34Ndipo Yehova anamva mau a kunena kwanu, nakwiya, nalumbira, ndi kuti, 35Palibe mmodzi wa anthu awa a mbadwo uno woipa adzaona dziko lokomalo ndinalumbira kupatsa makolo anuli. 36Koma Kalebi mwana wa Yefune, iye adzaliona; ndidzampatsa iye dziko limene anapondapo, ndi ana ace; popeza analimbika ndi kutsata Yehova. 37Yehova anakwiya ndi inenso cifukwa ca inu, ndi kuti, lwenso sudzalowamo. 38Yoswa mwana wa Nuni, wakuima pamaso pako, iye adzalowamo; umlimbitse mtima; popeza iye adzalandiritsa Israyeli. 39Ndipo ana anu amene mudanena, Adzakhala ogulidwa, ndi ana anu osadziwa cabwino kapena coipa ndi pano, iwo adzalowamo, ndidzawapatsa iwo ili, adzalilandira ndi iwo. 40Koma inu, bwererani, mukani ulendo wanu kucipululu, njira ya ku Nyanja Yofiira. 41Pamenepo munayankha ndi kunena ndi ine, Tacimwira Yehova, tidzakwera ndi kuthira mkhondo monga mwa zonse Yehova Mulungu wathu atiuza. Ndipo munadzimangira munthu yense zida zace za nkhondo, nimunakonzeka kukwera kumka kumapiri. 42Koma Yehova anati kwa ine, Nena nao, Musakwerako, kapena kuthira nkhondo; popeza sindiri pakati panu; angakukantheni adani anu. 43Pamene ndinanena ndi inu simunamvera; koma munatsutsana nao mau a Yehova ndi kucita modzikuza, nimunakwera kumka kumapiri. 44Ndipo Aamori, akukhala m'mapiri muja, anaturuka kukomana ndi inu, nakupitikitsani, monga zimacita njuci, nakukanthani m'Seiri, kufikira ku Horima. 45Ndipo munabwerera ndi kulira pamaso pa Yehova; koma Yehova sanamvera mau anu, kapena kukucherani khutu. 46Potero munakhala m'Kadesi masiku ambiri, monga mwa masiku munakhalako.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Deuteronomo 2

1Pamenepo tinabwerera, ndi kuyenda kumka kucipululu, kutsata
njira ya Nyanja Yofiira, monga Yehova adanena ndi ine; ndipo
tinapaza phiri la Seiri masiku ambiri. 2Ndipo Yehova ananena ndi
ine, ndi kuti, 3Yakwanira nthawi yakupaza inu phiri ili; tembenukani
kumka kumpoto, 4Ndipo uuze anthu, ndi kuti, Mukapite kubzyola
malire a abale anu, ana a Bsau okhala m'Seiri; ndipo adzakuopani;
mucenjere ndithu; 5musalimbana nao; popeza sindikupatsakoni
dziko lao, pangakhale popondapo phazi lanu ai pakuti ndapatsa
Bsau phiri la Seiri likhale lace lace. 6Mugulane nao cakudya ndi
ndarama, kuti mudye; mugulane naonso madzi kuti mumwe. 7Pakuti
Yehova Mulungu wanu anakudalitsani mu nchito zonse za manja
anu; anadziwa kuyenda kwanu m'cipululu ici cacikuru; zaka izi
makumi anai Yehova Mulungu wanu anakhala ndi inu; simunasowa
kanthu. 8Potero tinapitirira abale athu, ana a Bsau okhala m'Seiri,
njira ya cidikha, ku Elati ndi ku Ezioni Geberi.
9Pamenepo tinatembenuka ndi kudzera njira ya cipululu ca Moabu.
Ndipo Yehova anati kwa ine, Usabvuta Moabu, kapena kuutsana
naye nkhondo; popeza sindidzakupatsako dziko lace likhale lako
lako; pakuti ndinapatsa ana a Loti Ari likhale lao lao. 10(Aemi
anakhalamo kale, ndiwo anthu akuru, ndi ambiri, ndi atalitali, ngati
Aanaki. 11Anawayesa iwonso Arefai, monga Aanaki; koma Amoabu
awacha Aemi. 12Ndipo Ahori anakhala m'Seiri kale, koma ana a
Esau analanda dziko lao, nawaononga pamaso pao, nakhala
m'malo mwao; monga Israyeli anacitira dziko lace lace, limene
Yehova anampatsa.) 13Ukani tsopano, olokani mtsinje wa Zeredi.
Ndipo tinaoloka mtsinje wa Zeredi. 14Ndipo masiku amene
tinayenda kucokera ku Kadesi Barinea, kufikira tidaoloka mtsinje
wa Zeredi, ndiwo zaka makumi atatu mphambu zisanu ndi zitatu;
kufikira utatha mbadwo wonse wa amuna ankhondo m'cigono,
monga Yehova adawalumbirira. 15Komanso dzanja la Yehova
linatsutsana nao, kuwaononga m'cigono, kufikira adawatha.
16Ndipo kunali, atatha kufa amuna onse ankhondo mwa
anthu, 17Yehova ananena ndi ine, ndi kuti, 18Lero lomwe utumphe
malire a Moabu, ndiwo Ari. 19Ndipo pamene uyandikiza popenyana
ndi ana a Amoni, usawabvuta, kapena kuutsana nao; popeza
sindidzakupatsako dziko la ana a Amoni likhale lako lako; popeza
ndinapatsa ana a Loti ili likhale lao lao. 20(Ilinso aliyesa dziko la
Arefai; Arefai anakhalamo kale; koma Aamoni awacha
Azamzumi; 21ndiwo anthu akuru, ndi ambiri, ndi atalitali, monga
Aanaki; koma Yehova anawaononga pamaso pao; ndipo analanda
dziko lao, nakhala m'malo mwao; 22monga iye anacitira ana a
Bsau, akukhala m'Seiri, pamene anaononga Ahori pamaso pao;
ndipo analanda dziko lao, nakhala m'malo mwao kufikira lero

lomwe. 23Kunena za Aavi akukhala m'midzi kufikira ku Gaza,
Akafitori, akufuma ku Kafitori, anawaononga, nakhala m'malo
mwao.) 24Uka, yenda ulendo wako, ndi kuoloka mtsinje wa Arinoni;
taonani, ndapereka Sihoni mfumu ya Hesiboni, M-amori, ndi dziko
lace m'dzanja lako; yamba kulilandira, ndi kuutsana naye
nkhondo. 25Tsiku lino ndiyamba kuopsetsa nawe ndi kucititsa
mantha nawe anthu a pansi pa thambo lonse, amene adzamva
mbiri yako, nadzanjenjemera, nadzawawidwa cifukwa ca iwe.
26Ndipo ndinatuma amithenga ocokera ku cipululu ca Kedemoti
kwa Sihoni mfumu ya Hesiboni ndi mau a mtendere, ndi
kuti, 27Ndipitire m'dziko mwako; ndidzatsata mseu, osapatuka ine
ku dzanja lamanja kapena kulamanzere, 28Undigulitse cakudya ndi
ndarama, kuti ndidye; ndi kundipatsa madzi kwa ndarama, kuti
ndimwe; cokhaci ndipitire coyenda pansi; 29monga anandicitira
ana a Esau akukhala m'Seiri, ndi Amoabu akukhala m'Ari; kufikira
nditaoloka Yordano kulowa dziko limene Yehova Mulungu wathu
atipatsa. 30Koma Sihoni mfumu ya Hesiboni sanatilola kupitira
kwao; popeza Yehova Mulungu wanu anaumitsa mzimu wace,
nalimbitsa mtima wace, kuti ampereke m'dzanja lanu, monga lero
lino. 31Ndipo Yehova anati kwa ine, Taona, ndayamba kupereka
Sihoni ndi dziko lace pamaso pako; yamba kulandira dziko lace
likhale lako lako. 32Pamenepo Sihoni anaturuka kukomana nafe, iye
ndi anthu ace onse, kugwirana nafe nkhondo ku Yahaza. 33Ndipo
Yehova Mulungu wathu anampereka iye pamaso pathu; ndipo
tinamkantha, iye ndi ana ace amuna ndi anthu ace onse. 34Ndipo
muja tinalanda midzi yace yonse; ndipo tinaononga konse midzi
yonse, amuna ndi akazi ndi ana; sitinasiyapo ndi mmodzi
yense. 35Zoweta zokha tinadzifunkhira, pamodzi ndi zofunkha za
midzi tidailanda. 36Kuyambira ku Aroeri, ndiko kumphepete kwa
mtsinje wa Arinoni, ndi ku mudzi wokhala kumtsinje kufikira ku
Gileadi, kunalibe mudzi wakutitalikira malinga ace; Yehova
Mulungu wathu anapereka yonse pamaso pathu. 37Ku dziko la ana
a Amoni lokha simunayandikiza; dera lonse la mtsinje wa Yaboki,
ndi midzi ya kumapiri, ndi kwina kuli konse Yehova Mulungu wathu
anatiletsa.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Deuteronomo 3

1Pamenepo tinatembenuka, ndi kubwera kumka njira ya ku Basana;
ndipo Ogi mfumu ya Basana anaturuka kukomana nafe, kugwirana
nafe nkhondo, iye ndi anthu ace onse, ku Edrei. 2Ndipo Yehova anati
kwa ine, Usamuopa; popeza ndampereka iye ndi anthu ace onse,
ndi dziko lace, m'dzanja lako; umcitire monga umo unacitira Sihoni
mfumu ya Aamori, amene anakhala m'Hesiboni. 3Potero Yehova
Mulungu wathu anaperekanso m'manja mwathu Ogi mfumu ya
Basana, ndi anthu ace onse, ndipo tinamkantha kufikira
sanamtsalira ndi mmodzi yense. 4Ndipo muja tinalanda midzi yace
yonse; kunalibe mudzi sitinaulanda m'manja mwao, midzi makumi
asanu ndi limodzi, dera lonse la Arigobi, dziko la Ogi
m'Basana. 5Yonseyi ndiyo midzi yozinga ndi malinga atali, zitseko,
ndi mipiringidzo; pamodzi ndi midzi yambirimbiri yopanda
malinga. 6Ndipo tinaiononga konse, monga umo tinacitira Sihoni
mfumu ya Hesiboni, ndi kuononga konse midzi yonse, amuna, akazi
ndi ana. 7Koma zoweta zonse ndi zofunkha za m'midzi,
tinadzifunkhira tokha. 8Ndipo muja tinalanda dziko m'manja mwa
mafumu awiri a Aamori okhala tsidya lija la Yordano, kuyambira
mtsinje wa Arinoni kufikira phiri la Herimoni; 9(Asidoni alicha
Herimoni Sirioni, koma Aamori alicha Seniri); 10midzi yonse ya
kucidikha, ndi Gileadi lonse, ndi Basana lonse kufikira ku Saleka ndi
Edrei, midzi ya dziko la Ogi m'Basana. 11(Pakuti Ogi mfumu ya
Basana anatsala yekha wa iwo otsalira Arefai; taonani, kama wace
ndiye kama wacitsulo; sukhala kodi m'Raba wa ana a Amoni? utali
wace mikono isanu ndi inai, kupingasa kwace mikono inai, kuyesa
mkono wa munthu.) 12Ndipo dziko ili tinalilanda muja; kuyambira ku
Aroeri, wa ku mtsinje wa Arinoni, ndi dera lina la ku mapiri a Gileadi,
ndi midzi yace, ndinapatsa Arubeni ndi Agadi. 13Ndi cotsalira ca
Gileadi, ndi Basana lonse, dziko la Ogi, ndinapatsa pfuko la hafu la
Manase; dziko lonse la Arigobi, pamodzi ndi Basana. (Ndilo
lochedwa dziko la Arefai. 14Yairi mwana wa Manase analanda dziko
lonse la Arigobi, kufikira malire a Agesuri ndi Amaakati; nalicha
dzina lace, Basana Haroti Yairi, kufikira lero lino.) 15Ndipo
ndinampatsa Makiri Gileadi. 16Koma ndinapatsa Arubeni ndi Agadi
kuyambira ku Gileadi kufikira ku mtsinje wa Arinoni, pakati pa cigwa
ndi malire ace, kufikira mtsinje wa Yaboki, ndiwo malire a ana a
Amoni; 17ndi cidikha, ndi Yordano ndi malire ace, kuyambira ku
Kinerete kufikira ku nyanja ya kucidikha, ndiyo Nyanja ya Mcere,
patsinde pa Pisiga, kum'mawa.

18Ndipo ndinauza inu muja, ndi kuti, Yehova Mulungu wanu
wakupatsani dziko ili likhale lanu lanu, muoloke, amuna onse
amphamvu obvala zida zao, pamaso pa abale anu ana a
Israyeli. 19Koma akazi anu, ndi ana anu, ndi zoweta zanu,

(ndidziwa muli nazo zoweta zambiri), zikhale m'midzi yanu imene ndinakupatsani; 20kufikira Yehova atapumulitsa abale anu, monga anapumulitsa inu, nalandira iwonso dziko limene Yehova Mulungu wanu awapatsa tsidya lila la Yordano; pamenepo mudzabwerera munthu yense ku colowa cace, cimene ndinakupatsani. 21Ndipo ndinauza Yoswa muja, ndi kuti, Maso ako anapenya zonse Yehova Mulungu wanu anawacitira mafumu awa awiri; momwemo Yehova adzacitira maufumu onse kumene muolokerako. 22Musawaopa popeza Yehova Mulungu wanu, ndiye agwirira inu nkhondo. 23Ndipo ndinapempha cifundo kwa Yehova nthawi yomwe ija, ndi kuti, 24Ambuye Yehova, mwayamba Inu kuonetsera mtumiki wanu ukulu wanu, ndi dzanja lanu lamphamvu; pakuti Mulungu ndani m'mwamba kapena pa dziko lapansi wakucita monga mwa nchito zanu, ndi monga mwa mphamvu zanu? 25Ndioloketu, ndilione dziko lokomali liri tsidya la Yordano, mapiri okoma aja, ndi Lebano. 26Koma Yehova anakwiya ndi ine, cifukwa ca inu, sanandimvera ine; ndipo Yehova anati kwa ine, Cikukwanire, usaonjezenso kunena ndi Ine za cinthuci. 27Kwera kumwamba ku Pisiga, nukweze maso ako kumadzulo, ndi kumpoto, ndi kumwela, ndi kum'mawa, nuyang'ane ndi maso ako; popeza sudzaoloka Yordano uyo. 28Koma langiza Yoswa, dioloketu numlimbitse mtima, ndi kumkhwimitsa, pakuti adzaoloka pamaso pa anthu awa, nadzawalandiritsa dziko ulionali likhale lao lao. 29Potero tinakhala m'cigwamo pandunji pa Beti Peori.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Mose awadandaulira amvere Malamulo a Mulungu

1Ndipo tsopano, Israyeli, dioloketu tamverani malemba ndi
maweruzo, amene ndikuphunzitsani muwacite; kuti mukhale ndi
moyo, ndi kulowa, ndi kulandira dziko limene Yehova Mulungu wa
makolo anu akupatsani. 2Musamaonjeza pa mau amene
ndikuuzani, kapena kucotsapo, kuti musunge malamulo a Yehova
Mulungu wanu, amene ndikuuzani. 3Maso anu anapenya cocita
Yehova cifuwa ca Baala Peori; pakuti amuna onse amene anatsata
Baala Peori, Yehova Mulungu wanu anawaononga pakati
panu. 4Koma inu amene munamamatira Yehova Mulungu wanu
muli ndi moyo nonsenu lero lomwe. 5Taonani, ndinakuphunzitsani
malemba ndi maweruzo, monga Yehova Mulungu wanga anandiuza
ine, kuti muzicita cotero pakati pa dziko limene mumkako
kulilandira likhale lanu Lanu. 6Cifukwa cace asungeni, aciteni;
pakuti ici ndi nzeru zanu ndi cidziwitso canu pamaso pa mitundu
ya anthu akumva malemba ndi kuti, Ndithu mtundu waukuru uwu,
ndiwo anthu anzeru ndi akuzindikira. 7Pakuti dioloketu mtundu
waukuru wa anthu ndi uti, wakukhala ndi Mulungu pafupi pao
monga amakhala Yehova Mulungu wathu, pamene pali ponse
timaitanira iye? 8Ndipo mtundu waukuru wa anthu ndi uti,
wakukhala nao malemba ndi maweruzo olungama, akunga
cilamulo ici conse ndiciika pamaso panu lero lino? 9Cokhaci,
dzicenjerani nokha, ndi kusunga moyo wanu mwacangu, kuti
mungaiwale zinthuzi adaziona maso anu, ndi kuti zisacoke
kumtima kwanu masiku onse a moyo wanu; koma muzidziwitsa
ana anu ndi zidzukulu zanu. 10Tsikuli munaima pamaso pa Yehova
Mulungu wanu m'Horebe muja Yehova anati kwa ine,
Ndisonkhanitsire anthu, ndidzawamvetsa mau anga, kuti aphunzire
kundiopa Ine masiku ao onse akukhala ndi moyo pa dziko lapansi,
ndi kuti aphunzitse ana ao. 11Ndipo munayandikiza ndi kuima
patsinde pa phiri; ndi phizilo linayaka mota kufikira pakati pa
thambo; kunali mdima, ndi mtambo, inde mdima bii. 12Pamenepo
Yehova ananena ndi inu ali pakati pa moto; munamva kunena kwa
mau, osaona maonekedwe, koma kunenako. 13Pamenepo
anakufotokozerani cipangano cace, cimene anakulamulirani
kucicita, ndiwo Mau Khumi; nawalemba pa magome awiri
amiyala. 14Ndipo Yehova anandilamulira muja ndikuphunzitseni
malemba ndi maweruzo, kuti mukawacite m'dziko limene
muolokerako kulilandira likhale lanu lanu. 15Potero dzicenjerani nao
moyo wanu ndithu; popeza simunapenya mafanidwe konse tsikuli
Yehova ananena ndi inu m'Horebe, ali pakati pa moto; 16kuti
mungadziipse, ndi kudzipangira fano losema, lakunga cifaniziro ciri
conse, mafanidwe a mwamuna kapena mkazi; 17mafanidwe a

nyama iri yonse iri pa dziko lapansi, mafanidwe a mbalame iri yonse yamapiko yakuuluka m'mlengalenga, 18mafanidwe a cinthu ciri conse cokwawa pansi, mafanidwe a nsomba iri yonse yokhala m'madzi pansi pa dziko; 19ndi kuti mungakweze maso anu kupenya kumwamba, ndipo poona dzuwa ndi mwezi ndi nyenyezi, khamu lonse la kumwamba, munganyengedwe ndi kuzigwadira, ndi kuzitumikira, zimene Yehova Mulungu wanu anagawira mitundu yonse ya anthu pansi pa thambo lonse. 20Koma Yehova anakutengani, nakuturutsani m'ng'anjo yamoto, m'Aigupto, mukhale kwa iye anthu a colowa cace, monga mukhala lero lino. 21Yehova anakwiyanso nane cifukwa ca mau anu, nalumbira kuti sindidzaoloka Yordano ine, ndi kuti sindidzalowa m'dziko lokomali Yehova Mulungu wanu akupatsani likhale colowa canu; 22pakuti ndidzafa m'dziko muno, osaoloka Yordano; koma inu mudzaoloka, ndi kulandira dziko ili lokoma likhale lanu lanu. 23Dzicenjerani, mungaiwale cipangano ca Yehova Mulungu wanu, cimene anapangana nanu, ndi kuti mungadzipangire fano losema, cifaniziro ca kanthu kali konse Yehova Mulungu wanu anakuletsani. 24Pakuti Yehova Mulungu wanu ndiye moto wonyeketsa, ndi Mulungu wansanje.
25Mutakabala ana, ndi zidzukulu, ndipo mutakakhala nthawi yaikuru m'dzikomo, ndi kudziipsa, ndi kupanga fano losema, m'cifaniziro ca kanthu kali konse, ndi kucita coipa pamaso pa Yehova, kuutsa mkwiyo wace: 26ndiitana kumwamba ndi dziko lapansi zicite mboni pa inu lero lino, kuti mudzaonongeka msangatu kucotsedwa ku dziko limene muolokera Yordano kulilandira likhale lanu lanu; masiku anu sadzacuruka pamenepo, koma mudzaonongeka konse. 27Ndipo Yehova adzakubalalitsani mwa mitundu ya anthu, nimudzatsala pang'ono mwa amitundu, kumene Yehova adzakutsogolerani kwao. 28Ndipo kumeneko mudzatumikira milungu, nchito ya manja a anthu, mtengo ndi mwala, yosapenya, kapena kumva, kapena kudya, kapena kununkhiza. 29Koma mukafuna Yehova Mulungu wanu kumeneko, mudzampeza, ngati mumfunafuna ndi mtima wanu wonse ndi moyo wanu wonse. 30Mukakhala nao msauko, zikakugwerani zonsezi, masiku otsiriza mudzabwerera kwa Yehova Mulungu wanu ndi kumvera mau ace; 31popeza Yehova Mulungu wanu ndiye Mulungu wacifundo; sadzakusiyani, kapena kukuonongani, kapena kuiwala cipangano ca makolo anu cimene analumbirira iwo. 32Pakuti, funsiranitu, masiku adapitawo, musanakhale inu, kuyambira tsikuli Mulungu analenga munthu pa dziko lapansi, ndi kuyambira malekezero ena a thambo kufikira malekezero anzace a thambo, ngati cinthu cacikuru conga ici cinamveka, kapena kucitika? 33Kodi pali mtundu wa anthu udamva a Malungu akunena

pakati pa moto, monga mudamva inu, ndi kukhala ndi
moyo? 34Kapena kodi anayesa Mulungu kumuka ndi kudzitengera
mtundu mwa mtundu wina wa anthu, ndi mayesero, ndi zizindikilo,
ndi zozizwa, ndi nkhondo, ndi mwa dzanja lamphamvu, ndi mkono
wotambasuka, ndi mwa zoopsa zazikuru, monga mwa zonse
Yehova Mulungu wanu anakucitirani m'Aigupto pamaso
panu? 35Inu munaciona ici, kuti mudziwe kuti Yehova ndiye
Mulungu; palibe wina wopanda iye. 36Anakumvetsani mau ace
kucokera kumwamba, kuti akuphunzitseni; ndipo pa dziko lapansi
anakuonetsani moto wace waukuru; nimunamva mau ace pakati
pa moto. 37Ndipo popeza anakonda makolo anu, anasankha mbeu
zao zakuwatsata, nakuturutsani pamaso pace ndi mphamvu yace
yaikuru, m'Aigupto; 38kupitikitsa amitundu akuru ndi amphamvu
oposa inu pamaso panu, kukulowetsani ndi kukupatsani dziko lao
likhale colowa canu, monga lero lino. 39Potero dziwani lero tino
nimukumbukire m'mtima mwanu, kuti Yehova ndiye Mulungu,
m'thambo la kumwamba ndi pa dziko lapansi; palibe
wina. 40Muzisunga malemba ace, ndi malamulo ace, amene
ndikuzuzani lero lino, kuti cikukomereni inu ndi ana anu
akukutsatani, ndi kuti masiku anu acuruke pa dziko limene Yehova
Mulungu wanu akupatsani likhale lanu kosatha.

Midzi itatu yopulumukirako kum'mawa kwa Yordano

41Pamenepo Mose anapatula midzi itatu tsidya lija la Yordano
loturuka dzuwa; 42kuti athawireko wakupha munthu, osamupha
mnansi wace dala, osamkwiyira ndi kale lonse; ndi kuti, akathawira
ku umodzi wa midzi iyi, akhale ndi moyo: 43ndiyo Bezere,
m'cipululu, m'dziko lacidikha, ndiwo wa Anrubeni; ndi Ramoti
m'Gileadi, ndiwo wa Agadi; ndi Golani, m'Basana, ndiwo wa
Amanase. 44Ndipo ici ndi cilamulo Mose anaciika pamaso pa ana a
Israyeli; 45izi ndi mboni, ndi malemba, ndi maweruzo, Mose
anazinena kwa ana a Israyeli, poturuka iwo m'Aigupto; 46tsidya lija
la Yordano, m'cigwa ca pandunji pa Beti Peori, m'dziko la Sihoni
mfumu ya Aamori, wakukhala m'Hesiboni, amene Mose ndi ana a
Israyeli anamkantha, poturuka iwo m'Aigupto; 47ndipo analanda
dziko lace, ndi dziko la Ogi mfumu ya Basana, mafumu awiri a
Aamori, akukhala tsidya lija la Yordano loturuka
dzuwa; 48kuyambira ku Aroeri, ndiwo m'mphepete mwa mtsinje wa
Arinoni, kufikira phiri la Sioni (ndilo Herimoni), 49ndi cidikha conse
tsidya lija la Yordana kum'mawa, kufikira nyanja ya kucidikha, pa
tsinde lace la Pisiga.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Mose abwereza kuwachulira Malamulo a Mulungu

1Ndipo Mose anaitana Israyeli wonse, nanena nao, Tamverani, Israyeli, malemba ndi maweruzo ndinenawa m'makutu mwanu lero, kuti muwaphunzire, ndi kusamalira kuwacita. 2Yehova Mulungu wathu anapangana nafe cipangano m'Horebe. 3Yehova sanacita cipangano ici ndi makolo athu, koma ndi ife, ife amene tiri ndi moyo tonsefe pane lero. 4Yehova ananena ndi inu popenyana maso m'phirimo, ali pakati pa moto, 5(ndinalinkufma pakati pa Yehova ndi inu muja, kukulalikirani mau a Yehova; popeza munacita mantha cifukwa ca moto, osakwera m'phirimo) ndi kuti:
6Ine ndine Yehova Mulungu wako amene ndinakuturutsa m'dziko la Aigupto, m'nyumba ya akapolo.
7Usakhale nayo milungu yina koma Ine ndekha.
8Usadzipangire iwe wekha fano losema, kapena cifaniziro ciri conse ca zinthu za m'thambo la kumwamba, kapena za m'dziko lapansi, kapena za m'madzi a pansi pa dziko; 9usazipembedzere izo, usazitumikire izo; cifukwa Ine Yehova Mulungu wako ndine Mulungu wansanje, wakulanga ana cifukwa ca atate wao, kufikira mbadwo wacitatu ndi wacinai wa iwo amene akudana ndi Ine; 10ndi kucitira cifundo anthu zikwi, a iwo amene akondana ndi Ine nasunga malamulo anga.
11Usaehuledzinala Yehova Mulungu wako pacabe; cifukwa Yehova sadzamuyesa iye wosacimwa amene achula pacabe dzina lacelo.
12Samalira tsiku la Sabata likhale lopatulika, monga Yehova Mulungu wako anakulamulira. 13Masiku asanu ndi limodzi uzigwiritsa nchito, ndi kucita nchito zako zonse; 14koma tsiku lacisanu ndi ciwiri ndilo Sabata la Yehova Mulungu wako; usamagwira nchito iri yonse, iwe, kapena mwana wako wamwamuna, kapena mwana wako wamkazi, kapena wanchito wako wamwamuna, kapena wanchito wako wamkazi, kapena ng'ombe yako, kapena buru wako, kapena zoweta zako ziri zonse, kapena mlendo wokhala m'mudzi mwako; kuti wanchito wako wamwamuna ndi wanchito wako wamkazi apumule monga iwe mwini. 15Ndipo uzikumbukilakuti unali kapolo m'dziko la Aigupto, ndi kuti Yehova Mulungu wako anakuturutsako ndi dzanja lamphamvu ndi mkono wotambasuka; cifukwa cace Yehova Mulungu wako anakulamulira kusunga tsiku la Sabata.
16Lemekeza atate wako ndi amako, monga Yehova Mulungu wako anakulamulira; kuti masiku ako acuruke, ndi kuti cikukomere, m'dziko limene Yehova Mulungu wako akupatsa iwe.
17Usaphe.
18Usacite cigololo.
19Usabe.

20Usamnamizire mnzako.
21Usasirire mkazi wace wa mnzako; usakhumbe nyumba yace ya
mnzako, munda wace, kapena wanchito wace wamwamuna,
kapena wanchito wace wamkazi, ng'ombe yace, kapena buru
wace, kapena kanthu kali konse ka mnzako.
22Yehova ananena mau awa kwa msonkhano wanu wonse,
m'phirimo ali pakati pa moto, pamtambo, pamdima bii, ndi mau
akuru; osaonjezapo kanthu. Ndipo anawalembera pa magome awiri
amiyala, nandipatsa awa. 23Ndipo kunali, pamene munamva liu
loturuka pakati pa mdima, potentha phiri ndi moto, munayandikiza
kwa ine, ndiwo mafumu onse a mapfuko anu ndi akuru
anu; 24ndipo munati, Taonani, Yehova Mulungu wathu anationetsa
ulemerero wace, ndi ukuru wace, ndipo tidamva liu lace ali pakati
pa mote; tapenya lero lino kuti Mulungu anena ndi munthu, ndipo
akhala ndi moyo. 25Ndipo tsopano tiferenji? popeza mote waukuru
uwu udzatitha. Tikaonjeza kumva mau a Yehova Mulungu wathu,
tidzafa. 26Pakuti ndaniyo, wa zamoyo zonse adamva mau a
Mulungu wamoyo wakunena ali pakati pa moto, monga ife,
nakhala ndi moyo? 27Yandikizani inu, ndi kumva zonse Yehova
Mulungu wathu adzati; ndipo inu munene ndi ife zonse zimene
Yehova Mulungu wathu adzanena ndi inu; ndipo ife tidzazimva ndi
kuzicita. 28Ndipo Yehova anamva mau a kunena kwanu, pamene
munanena ndi ine; ndipo Yehova anati kwa ine, Ndidamva mau a
kunena kwao kwa anthu awa, amene ananena ndi iwe; cokoma
cokha cokha adanenaci. 29Ha! mwenzi akadakhala nao mtima
wotere wakundiopa Ine, ndi kusunga malamulo anga masiku onse,
kuti ciwakomere iwo ndi ana ao nthawi zonse! 30Muka, nuti nao,
Bwererani ku mahema anu. 31Koma iwe, uime kuno ndi Ine,
ndinene ndi iwe malamulo onse, ndi malemba, ndi maweruzo,
amene uziwaphunzitsa, kuti awacite m'dziko limene ndiwapatsa
likhale lao lao. 32Potero muzisamalira kucita monga Yehova
Mulungu wanu anakulamulirani; musamapatuka kulamanzere
kapena kulamanja. 33Muziyenda m'njira yonse imene Yehova
Mulungu wanu anakulamulirani, kuti mukakhale ndi moyo, ndi kuti
cikukomereni, ndi kuti masiku anu acuruke m'dziko limene
mudzakhala nalo lanu lanu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Awapempha asunge Malamulo a Mulungu kuti adale

1Ndipo awa ndi malamulo, malemba, ndi maweruzo, amene
Yehova Mulungu wanu analamulira kukuphunzitsani, kuti
muziwacita m'dziko limene muolokerako kulilandira; 2kuti muope
Yehova Mulungu wanu, kusunga malemba ace onse ndi malamulo
ace, amene ndikuuzani inu ndi ana anu, ndi zidzukulu zanu, masiku
onse a moyo wanu, ndi kuti masiku anu acuruke. 3Potero imvani,
Israyeli, musamalire kuwacita, kuti cikukomereni ndi kuti mucuruke
cicurukire, monga Yehova Mulungu wa makolo anu anena ndi inu,
m'dziko moyenda mkaka ndi uci ngati madzi.
4Imvani, Israyeli; Yehova Mulungu wathu, Yehova ndiye
mmodzi; 5ndipo muzikonda Yehova Mulungu wanu ndi mtima wanu
wonse, ndi moyo wanu wonse, ndi mphamvu yanu yonse. 6Ndipo
mau awa ndikuuzanilero, azikhala pamtima panu; 7ndipo
muziwaphunzitsa mwacangu kwa ana anu, ndi kuwalankhula awa
pokhala pansi m'nyumba zanu, ndi poyenda inu panjira, ndi
pogona inu pansi, ndi pouka inu. 8Ndipo muziwamanga padzanja
panu ngati cizindikilo, ndipo akhale ngati capamphumi pakati pa
maso anu. 9Ndipo muziwalembera pa mphuthu za nyumba zanu,
ndi pa zipata zanu. 10Ndipo kudzakhala, Yehova Mulungu wanu
atakulowetsani m'dziko limene analumbirira makolo anu,
Abrahamu, Isake, ndi Yakobo, kuti adzakupatsani ili; midzi yaikuru
ndi yokoma, imene simunaimanga; 11ndi nyumba zodzala nazo
zokoma ziri zonse, zimene simunazidzaza, ndi zitsime zosema,
zimene simunazisema, minda yampesa, ndi minda yaazitona,
zimene simunazioka, ndipo mutakadya ndi kukhuta; 12pamenepo
mudzicenjere mungaiwale Yehova, amene anakuturutsani m'dziko
la Aigupto, m'nyumba ya akapolo, 13Muziopa Yehova Mulungu
wanu; ndi kutumikira Iyeyu; ndipo polumbira muzichula dzina
lace. 14Musamatsata milungu yina, milungu yina ya mitundu ya
anthu akuzinga inu; 15pakuti Yehova Mulungu wanu ali pakati panu,
ndiye Mulungu wansanje; kuti ungapse mtima wa Yehova Mulungu
wanu, ndi kukuonongani, kukucotsani pankhope pa dziko lapansi.
16Musamayesa Yehova Mulungu wanu, monga munamyesa
m'Masa. 17Muzisunga mwacangu malamulo a Yehova Mulungu
wanu, ndi mboni zace, ndi malemba ace, amene
anakulamulirani. 18Ndipo muzicita zolunjika ndi zokoma pamaso pa
Yehova; kuti cikukomereni, ndi kuti mulowe kukalandira dziko
lokomali Yehova analumbirira makolo anu, 19kuingitsa adani anu
onse pamaso panu, monga Yehova adanena.
20Akakufunsani ana anu m'tsogolomo, ndi kuti, Mbonizo, ndi
malemba, ndi maweruzo, zimene Yehova Mulungu wathu
anakulamulirani, zitani? 21Pamenepo muzinena kwa ana anu, Tinali

akapolo a Farao m'Aigupto; ndipo Yehova anatiturutsa m'Aigupto
ndi dzanja lamphamvu. 22Ndipo Yehova anapatsa zizindikilo ndi
zozizwa zazikuru ndi zowawa m'Aigupto, pa Farao, ndi pa nyumba
yace yonse, pamaso pathu; 23ndipo anatiturutsa komweko, kuti
atilowetse, kutipatsa dzikoli analumbirira makolo athu. 24Ndipo
Yehova anatilamulira tizicita malemba awa onse, kuopa Yehova
Mulungu wathu, kuti tipindule nako masiku onse, kuti atisunge
amoyo, monga lero lino. 25Ndipo kudzakhala kwa ife cilungamo,
ngati tisamalira kucita malamulo awa onse pamaso pa Yehova
Mulungu wathu, monga anatilamuliraife.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Awapangira za Akanani ndi zipembedzo zao

1Pamene Yehova Mulungu wanu atakulowetsani m'dziko limene
mumkako kulilandira likhale lanu lanu, ndipo atakataya amitundu
ambiri pamaso panu, Ahiti, ndi Agirigazi, ndi Aamori, ndi Akanani,
ndi Aperizi, ndi Ahivi, ndi Ayebusi, mitundu isanu ndi iwiri yaikuru
ndi yamphamvu yoposa inu; 2nakawapereka Yehova Mulungu wanu
pamaso panu, ndipo mukawakanthe; pamenepo muwaononge
konse; musapangana nao pangano, kapena kuwacitira
cifundo. 3Ndipo musakwatitsane nao; musampatsemwana wace
wamwamuna mwana wanu wamkazi, kapena kutenga mwana
wace wamkazi akhale wa mwana wanu wamwamuna. 4Popeza
adzapatutsa mwana wanu aleke kunditsata Ine, kuti atumikire
milungu yina; potero Yehova adzapsa mtima pa inu, ndipo
adzakuononga ni msanga. 5Koma muzicita nao motero: mukapasule
maguwa ao a nsembe, ndi kuphwanya zoimiritsa zao, ndi kulikha
zifanizo zao, ndi kutentha mafano ao osema ndi moto. 6Pakuti inu
ndinu mtundu wa anthu wopatulika wa Yehova Mulungu wanu;
Yehova Mulungu wanu anakusankhani, mukhale mtundu wa pa
wokha wa iye yekha, mwa mitundu yonse ya anthu akukhala pa
nkhope ya dziko. 7Yehova sanakondwera nanu, ndi kukusankhani
cifukwa ca kucuruka kwanu koposa mitundu yonse yina ya anthu,
kapena kucepera kwanu; 8koma Yehova anakuturutsani ndi dzanja
lamphamvu, ndi kukuombolani m'nyumba ya akapolo, m'dzanja la
Farao mfumu ya Aigupto, cifukwa Yehova akukondani, ndi cifukwa
ca kusunga lumbiro lija analumbirira makolo anu. 9Cifukwa cace
dziwani kuti Yehova Mulungu wanu ndiye Mulungu; ndiye Mulungu
wokhulupirika, wakusunga cipangano ndi cifundo ndi iwo
akumkonda ndi kusunga malamulo ace, kufikira mibadwo
zikwi. 10Ndipo awabwezera onse akudana ndi iye, pamaso pao,
kuwaononga; sacedwa naye wakudana ndi iye, ambwezera
pamaso pace. 11Potero muzisunga malamulo, ndi malemba, ndi
maweruzo, amene ndikuuzani lero kuwacita.
12Ndipo kudzakhala, cifukwa ca kumvera inu maweruzo awa, ndi
kuwasunga, ndi kuwacita, Yehova Mulungu wanu adzakusungirani
cipangano ndi cifundo cimene analumbirira makolo anu; 13ndipo
adzakukondani, ndi kukudalitsani, ndi kukucurukitsani;
adzadalitsanso zipatso za thupi lanu, ndi zipatso za nthaka yanu,
tirigu wanu, ndi vinyo wanu, ndi mafuta anu, zoswana za ng'ombe
zanu, ndi ana a nkhosa anu, m'dziko limene analumbirira makolo
anu kuti adzakupatsani. 14Mudzakhala odalitsika koposa mitundu
yonse ya anthu; sipadzakhala mwamuna kapena wamkazi
wosabala pakati pa inu, kapena pakati pa zoweta zanu. 15Ndipo
Yehova adzakucotserani nthenda zonse; sadzakuikirani nthenda

zoipa ziri zonse za Aigupto muzidziwa zija; koma adzaziika pa onse
akudana ndi inu. 16Ndipo mudzatha mitundu yonse ya anthu
amene Yehova Mulungu wanu adzapereka kwa inu; diso lanu
lisawacitire cifundo; musamatumikira milungu yao; pakuti uku
kudzakucitirani msampha. 17Mukadzanena m'mtima mwanu,
Amitundu awa andicurukira; ndikhoza bwanji
kuwapitikitsa? 18musamawaopa; mukumbukile bwino cimene
Yehova Mulungu wanu anacitira Farao, ndi Aigupto
wonse; 19mayesero akuru maso anu anawapenya, ndi zizindikilo
ndi zozizwa, ndi dzanja lamphamvu, ndi mkono wotambasuka,
zimene Yehova Mulungu wanu anakuturutsani nazo; Yehova
Mulungu wanu adzatero nayo mitundu yonse ya anthu imene
muwaopa. 20Komanso Yehova Mulungu wanu adzatumiza mabvu
pakati pao, kufikira ataonongeka otsalawo, ndi akubisala pamaso
panu. 21Musamaopa pamaso pao; popeza Yehova Mulungu wanu
ali pakati pa inu, Mulungu wamkuru ndi woopsa. 22Ndipo Yehova
Mulungu wanu adzataya amitundu awa pang'ono pang'ono;
simuyenera kuwaononga msanga, kuti zingakucurukireni
zirombo. 23Koma Yehova Mulungu wanu adzawapereka pamaso
panu, nadzawapitikitsa ndi kupitikitsa kwakukuru, kufikira
ataonongeka. 24Adzaperekanso mafumu ao m'dzanja mwanu,
ndipo muwafafanize maina ao pansi pa thambo; palibe munthu
mmodzi adzaima pamaso panu, kufikira mutawaononga, 25Mafano
osema a milungu yao muwateothe ndi moto; musamasirira siliva
ndi golidi ziri pa iwo, kapena kudzitengera izi; mungakodwe nazo;
pakuti izi zinyansira Yehova Mulungu wanu. 26Musamalowa naco
conyansaci m'nyumba mwanu, kuti mungaonongeke konse
pamodzi naco; muziipidwa naco konse, ndi kunyansidwa naco
konse; popeza ndi cinthu coyenera kuonongeka konse.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Akumbuke zokoma zazikuru Mulungu anawacitira

1Muzisamalira kucita malamulo onse amene ndikuuzani lero lino,
kuti mukhale ndi moyo, ndi kucuruka, ndi kulowa, ndi kulandira
dziko limene Yehova analumbirira makolo anu. 2Ndipo
mukumbukile njira yonse imene Yehova Mulungu wanu
anakuyendetsani m'cipululu zaka izi makumi anai, kuti
akucepetseni, kukuyesani, kudziwa cokhala mumtima mwanu,
ngati mudzasunga malamulo ace, kapena iai. 3Ndipo
anakucepetsani, nakumvetsani odala, nakudyetsani ndi mana,
amene simunawadziwa, angakhale makolo anu sanawadziwa; kuti
akudziwitseni kuti munthu sakhala wamoyo ndi mkate wokha,
koma munthu akhala wamoyo ndi zonse zakuturuka m'kamwa
mwa Yehova. 4Zobvala zanu sizinatha pathupi panu, phazi lanu
silinatupa zaka izi makumi anai. 5Ndipo muzindikire m'mtima
mwanu, kuti monga munthu alanga mwana wace, momwemo
Yehova Mulungu wanu akulangani inu. 6Ndipo muzisunga
malamulo a Yehova Mulungu wanu, kuyenda m'njira zace, ndi
kumuopa. 7Pakuti Yehova Mulungu wanu akulowetsani m'dziko
lokoma, dziko la mitsinje yamadzi, la akasupe, ndi la maiwe
akuturuka m'zigwa, ndi m'mapiri; 8dziko la tirigu ndi barele, ndi
mipesa, ndi mikuyu, ndi makangaza; dziko la azitona a mafuta, ndi
uci; 9dziko loti mudzadyamo mkate wosapereweza;
simudzasowamo kanthu; dziko loti miyala yace nja citsulo, ndi
m'mapiri ace mukumbe mkuwa. 10Ndipo mudzadya ndi kukhuta,
ndi kuyamika Yehova Mulungu wanu cifukwa ca dziko lokomali
anakupatsani. 11Cenjerani mungaiwale Yehova Mulungu wanu, ndi
kusasunga malamulo ace, ndi maweruzo ace, ndi malemba ace,
amene ndikuuzani lero lino; 12kuti, mutadya ndi kukhuta, ndi
kumanga nyumba zokoma, ndi kukhalamo; 13ndipo zitacuruka
ng'ombe zanu, ndi nkhosa zanu, zitacurukanso siliva wanu ndi
golidi wanu, zitacurukanso zonse muli nazo; 14mtima wanu
ungatukumuke, nimungaiwale Yehova Mulungu wanu, amene
anakuturutsani m'dziko la Aigupto, m'nyumba ya
akapolo; 15amene anakutsogolerani m'cipululu cacikuru ndi
coopsaco, munali njoka zamoto, ndi zinkhanira, mouma mopanda
madzi; amene anakuturutsirani madzi m'thanthwe
lansangalabwi; 16amene anakudyetsani m'cipululu ndi mana,
amene makolo anu sanawadziwa; kuti akucepetseni, ndi kuti
akuyeseni, kuti akucitireni cokoma potsiriza panu; 17ndipo
munganene m'mtima mwanu, Mphamvu yanga ndi mkono wanga
wolimba zinandifunira cuma ici. 18Koma mukumbukile Yehova
Mulungu wanu, popeza ndi Iyeyu wakupatsani mphamvu
yakuonera cuma; kuti akhazikitse cipangano cace cimene

analumbirira makolo anu, monga cikhala lero lino. 19Ndipo
kudzakhala kuti mukaiwalatu Yehova Mulungu wanu, ndi kutsata
milungu yina ndi kuitumikira, ndikucitirani mboni lero lino kuti
mudzaonongeka ndithu. 20Monga amitundu amene Yehova
awaononga pamaso panu, momwemo mudzaonongeka; cifukwa ca
kusamvera mau a Yehova Mulungu wanu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Deuteronomo 9

1Imvani Israyeli; mulikuoloka Yordano lero lino, kulowa ndi kulandira amitundu akuru ndi amphamvu akuposa inu, midzi yaikuru ndi ya malinga ofikira kuthambo, 2anthu akuru ndi atalitali, ana a Aanaki, amene muwadziwa, amene munamva mbiri yao, ndi kuti, Adzaima ndani pamaso pa ana a Anaki? 3Potero mudziwe lero lino, kuti Yehova Mulungu wanu ndiye amene aoloka pamaso panu ngati moto wonyeketsa; iye adzawaononga, iye adzawagwetsa pamaso panu; potero mudzawapitikitsa, ndi kuwaononga msanga, monga Yehova analankhula ndi inu. 4Musamanena mumtima mwanu, atawapitikitsa pamaso panu Yehova Mulungu wanu, ndi kuti, Cifukwa ca cilungamo canga Yehova anandilowetsa kudzalandira dziko ili; pakuti Yehova awapitikitsa pamaso panu cifukwa ca zoipa za amitundu awa. 5Simulowa kulandira dziko lao cifukwa ca cilungamo canu, kapena mtima wanu woongoka; koma Yehova Mulungu wanu awapitikitsa pamaso panu cifukwa ca zoipa za amitundu awa, ndi kuti akhazikitse mau amene Yehova analumbirira makolo anu, Abrahamu, ndi Isake, ndi Yakobo. 6Potero mudziwe, kuti Yehova Mulungu wanu sakupatsani dziko ili lokoma mulilandire, cifukwa ca cilungamo canu; pakuti inu ndinu mtundu wa aathu opulukira. 7Kumbukilani, musamaiwala, kuti munakwiyitsa Yehova Mulungu wanu m'cipululu; kuyambira tsikuli munaturuka m'dziko la Aigupto, kufikira munalowa m'malo muno munapiktsana ndi Yehova. 8M'Horebe momwe munautsa mkwiyo wa Yehova; ndipo Yehova anakwiya nanu kukuononganí. 9Muja ndinakwera m'phiri kukalandira ma gome amiyala, ndiwo magome a cipangano cunene Yehova anapangana ndi inu, ndinakhala m'phiri masiku makumi anai usana ndi usiku; osadya mkate osamwa madzi. 10Ndipo Yehova anapereka kwa ine magome awiri amiyala, olembedwa ndi cala ca Mulungu; ndipo panalembedwa pamenepo monga mwa mau onse amene Yehova adanena ndi inu m'phirimo, ali pakati pa moto, tsiku lakusonkhana. 11Ndipo kunali, atatha masiku makumi anai usana ndi usiku, kuti Yehova anandipatsa magome awiriwo amiyala, ndiwo magome a cipangano, 12Ndipo Yehova anati kwa ine, Uka, fulumira kutsika kuno popeza anthu ako unawaturutsa m'Aigupto wa anadziipsa; anapatuka msanga m'njira ndinawalamulirayi; anadzipangira fano loyenga. 13Yehova ananenanso ndi ine, ndi kuti, Ndapenya anthu awa, taona, awa ndi anthu opulukira; 14undileke, ndiwaononge, ndi kufafaniza dzina lao pansi pa thambo; ndipo ndidzakuyesa iwe mtundu wa anthu wamphamvu ndi waukuru woposa iwo. 15Pamenepo ndinatembenuka ndi kutsika m'phiri, ndi phirilo linatentha ndi moto; ndi magome awiri a cipangano anali m'manja mwanga. 16Ndipo ndinapenya, taonani, mudacimwira Yehova Mulungu wanu; mudadzipangira mwana wa ng'ombe

woyenga; mudapatuka msanga m'njira imene Yehova adalamulira inu. 17Pamenepo ndinagwira magome awiriwo, ndi kuwataya acoke m'manja anga awiri, ndi kuwaswa pamaso panu. 18Ndipo ndinagwa pansi pamaso pa Yehova, monga poyamba paja, masiku makumi anai usana ndi usiku, osadya mkate osamwa madzi, cifukwa ca macimo anu onse mudacimwa, ndi kucita coipaco pamaso pa Yehova, kuutsa mkwiyo wace. 19Pakuti ndinacita mantha cifukwa ca mkwiyo waukali, umene Yehova anakwiya nao pa inu kukuonongani, Koma Yehova anandimvera nthawi ijanso. 20Ndipo Yehova aliakwiya kwambiri ndi Aroni kumuononga; koma ndinampempherera Aroni nthawi yomweyo. 21Ndipo ndinatenga cimo lanu, mwana wa ng'ombe mudampangayo, ndi kumtentha ndi moto, ndi kumphwanya, ndi kumpera bwino kufikira atasalala ngati pfumbi; ndipo ndinataya pfumbi lace m'mtsinje wotsika m'phirimo. 22Ku Tabera, ndi ku Masa, ndi ku Kibiroti Hatava, munautsanso mkwiyo wa Yehova. 23Ndipo pamene Yehova anakutumizani kucokera ku Kadesi Barinea, ndi kuti, Kwerani, landirani dziko limene ndakupatsani; munapikisana nao mau a Yehova Mulungu wanu, osamkhulupirira, kapena kumvera mau ace. 24Munakhala opikisana ndi Yehova kuyambira tsikuli ndinakudziwani. 25Ndipo ndinagwa pansi pamaso pa Yehova masiku makumi anai usana ndi usiku ndinagwa pansiwa; popeza Yehova adati kuti adzakuonongani. 26Ndipo ndinapemphera kwa Yehova ndi kuti, Yehova Mulungu, musaononga anthu anu ndi colowa canu, amene mudawaombola mwa ukulu wanu, amene munawaturutsa m'Aigupto ndi dzanja lamphamvu, 27Kumbukilani atumiki anu, Abrahamu, Isake, ndi Yakobo; musapenyerera kupulukira kwa anthu awa, kapena coipa cao, kapena cimo lao; 28kuti linganene dziko limene mudatiturutsako, Popeza Yehova sanakhoza kuwalowetsa m'dziko limene adanena nao, ndi popeza anadana nao, anawaturutsa kuti awaphe m'cipululu. 29Koma iwo ndiwo anthu anu ndi colowa canu, amene mudaturutsa ndi mphamvu yanu yaikuru ndi dzanja lanu lotambasuka.
©The Bible Society of Malawi, 1992

Za magome aciwiri a Malamulo

1Masiku aja Yehova anati kwa ine, Dzisemere magome awiri
amiyala onga oyamba aja, nukwere kuno kwa Ine m'phiriumu,
nudzipangire likasa lamtengo. 2Ndipo ndidzalembera pa
magomewo mauwo anali pa magome oyamba aja amene
unawaswa, ndipo uwaike m'likasamo. 3Potero ndinapanga likasa la
mtengo wasitimu, ndinasemanso magome awiri amiyala onga
oyamba aja, ndi kukwera m'phirimo, magome awiri ali m'manja
mwanga. 4Ndipo analembera pamagome, monga mwa
malembedwe oyamba, mau khumiwo, amene Yehova adanena ndi
inu m'phirimo, ali pakati pa moto, tsiku la kusonkhanako; ndipo
Yehova anandipatsa awa. 5Ndipo ndinatembenuka ndi kutsika
m'phiri, ndi kuika magome m'likasa ndinalipanga, ali m'menemo
monga Yehova anandilamulira ine. 6Ndipo ana a Israyeli anayenda
ulendo wao kucokera ku zitsime za ana a Yaakani kufikira ku
Mosera. Kumeneko anamwalira Aroni, ndi kumeneko anamuika;
ndipo Eleazara mwana wace anacita nchito ya nsembe m'malo
mwace. 7Kucokerako anamka ulendo ku Gudigoda, ndi kucokera ku
Gudigoda kumka ku Yotibata, dziko la mitsinje yamadzi. 8Masiku
aja Yehova anapatula pfuko la Levi, linyamule likasa la cipangano
la Yehova, liimirire pamaso pa Yehova kumtumikira, ndi kudalitsa
m'dzina lace kufikira lero lino. 9Cifukwa cace Levi alibe gawo
kapena colowa pamodzi ndi abale ace; Yehova mwini wace ndiye
colowa cace, monga Yehova Mulungu wace ananena naye. 10Ndipo
ndinakhala m'phiri monga poyamba paja, masiku makumi anai
usana ndi usiku; ndipo Yehova anandimvera ine pameneponso;
Yehova sanafuna kukuonongani. 11Ndipo Yehova anati kwa ine,
Uka, tenga ulendo pamaso pa anthu; kuti alowe ndi kulandira
dzikoli ndinalumbirira makolo ao kuti ndidzawapatsa.

Abwereza kuwadandaulira akonde namvere Mulungu

12Ndipo tsopano, Israyeli, Yehova Mulungu wanu afunanji nanu,
koma kuti muziopa Yehova Mulungu wanu, kuyenda m'njira zace
zonse, ndi kukonda, ndi kutumikira Yehova Mulungu wanundimtima
wanu wonse ndi moyo wanu wonse, 13kusunga malamulo a
Yehova, ndi malemba ace, amene ndikuuzani lero kuti
kukukomereni inu? 14Taonani thambo, ndi kumwambamwamba,
dziko lapansi, ndi zonse ziri m'mwemo ndi zace za Yehova Mulungu
wanu. 15Koma Yehova anakondwera nao makolo anu kuwakonda,
nasankha mbeu zao zakuwatsata, ndiwo inu, mwa mitundu yonse
ya anthu, monga kuli lero lino. 16Potero dulani khungu la mitima
yanu, ndipo musamapulukiranso. 17Popeza Yehova Mulungu wanu
ndiye Mulungu wa milungu, ndi Mbuye ya ambuye; Mulungu
wamkuru, wamphamvu, ndi woopsa, wosasamalira nkhope za

anthu, kapena kulandira cokometsera mlandu. 18Aweruzira ana amasiye ndi mkazi wamasiye; ndipo akonda mlendo, ndi kumpatsa cakudya ndi cobvala. 19M'mwemo mukondane naye mlendo; popeza munali alendo m'dziko la Aigupto. 20Muziopa Yehova Mulungu wanu; mumtumikire Iyeyo; mummamatire iye, ndi kulumbira pa dzina lace. 21Iye ndiye lemekezo lanu, Ive ndiye Mulungu wanu, amene anacita nanu zazikuru ndi zoopsa izi, mudaziona m'maso mwanu. 22Makolo anu anatsikira ku Aigupto ndiwo anthu makumi asanu ndi awiri; ndipo Yehova Mulungu wanu anakusandulizani tsopano mucuruke ngati nyenyezi za kumwamba.

©The Bible Society of Malawi, 1992

1Cifukwa cace muzikonda Yehova Mulungu wanu, ndi kusunga
cilangizo cace, ndi malemba ace, ndi maweruzo ace, ndi malamulo
ace, masiku onse. 2Ndipo dziwani lero lino; pakuti sindinena ndi ana
anu osadziwa, ndi osapenya kulanga kwa Yehova Mulungu wanu,
ukulu wace, dzanja lace lamphamvu, ndi mkono wace
wotambasuka, 3ndi zizindikilo zace, ndi nchito zace, adazicitira
Farao mfumu ya Aigupto, ndi dziko lace lonse pakati pa
Aigupto; 4ndi cocitira iye nkhondo ya Aigupto, akavalo ao, ndi
agareta ao; kuti anawamiza m'madzi a Nyanja Yofiira, muja
anakutsatani m'mbuyo, ndi kuti Yehova anawaononga kufikira lero
lino; 5ndi cimene anakucitirani m'cipululu, kufikira munadza kumalo
kuno; 6ndi cimene anacitira Datani ndi Abiramu, ana a Eliabu,
mwana wa Rubeni; muja nthaka inatsegula pakamwa pace, ndi
kuwameza iwo, ndi mabanja ao, ndi mahema ao, ndi za moyo zonse
zakuwatsata pakati pa Israyeli wonse. 7Koma maso anu anapenya
nchito yonse yaikuru ya Yehova anaicita. 8Potero muzisunga
malamulo onsewa ndikuuzani lero lino, kuti mukhale amphamvu,
ndi kulowa ndi kulandira dziko, limene mumkako kulilandira; 9ndi
kuti masiku anu acuruke m'dziko limene Yehova analumbirira
makolo anu, kuti adzawapatsa iwo ndi mbeu zao, dziko moyenda
mkaka ndi uci ngati madzi. 10Pakuti dziko limene mumkako
kulilandira ndi losanga dziko la Aigupto lija mudaturukako, kumene
kuja munafesa mbeu zanu, ndi kuzithirira ndi phazi lanu, monga
munda watherere; 11koma dziko limene mumkako kulilandira ndilo
dziko la mapiri ndi zigwa; limamwa madzi a mvula ya
kumwamba; 12ndilo dziko loti Yehova Mulungu wanu alisamalira,
maso a Yehova Mulungu wanu akhalapo cikhalire, kuyambira caka
mpaka kutsiriza caka.

Za madalitso otsatira kumvera kwao

13Ndipo kudzakhala mukasamalira cisamalire malamulo anga
amene ndikuuzani lero lino, kukonda Yehova Mulungu wanu, ndi
kumtumikira ndi mtima wanu wonse, ndi moyo wanu
wonse, 14ndidzapatsa mvula ya dziko lanu m'nyengo yace, ya
myundo ndi ya masika, kuti mutute tirigu wanu, ndi vinyo wanu,
ndi mafuta anu. 15Ndipo ndidzapatsa msipu wa zoweta zanu
podyetsa panu; mudzadyanso nimudzakhuta. 16Dzicenjerani
nokha, angacete mitima yanu, nimungapatuke, ndi kutumikira
milungu yina, ndi kuipembedza; 17ndi kuti Mulungu angapse mtima
pa inu, a nangatseke kumwamba, kuti isowe mvula, ndi kuti nthaka
isapereke zipatso zace; ndi kuti mungaonongeke msanga m'dziko
lokomali Yehova akupatsani. 18Cifukwa cace muzisunga mau anga
awa mumtima mwanu ndi m'moyo mwanu; ndi kuwamanga ngati
cizindikilo pamanja panu; ndipo zikhale zapamphumi pakati pa

maso anu. 19Ndipo muziwaphunzitsa ana anu, ndi kuwalankhula
awa pokhala inu pansi m'nyumba mwanu, ndi poyenda inu panjira,
ndi pogona inu pansi, ndi pakuuka inu pomwe. 20Ndipo
muziwalembera pa mphuthu za nyumba zanu, ndi pa zipata
zanu; 21kuti masiku anu ndi masiku a ana anu acuruke m'dziko
limene Yehova analumbira kwa makolo anu kuti adzawapatsali,
monga masiku a thambo liri pamwamba pa dziko. 22Pakuti
mukasunga cisungire malamulo awa onse amene ndikuuzani
kuwacita; kukonda Yehova Mulungu wanu, kuyenda m'njira zace
zonse, ndi kummamatira; 23Yehova adzapitikitsa amitundu awa
onse pamaso panu, ndipo mudzalanda amitundu akuru ndi
amphamvu oposa inu. 24Pamalo ponse padzapondapo phazi lanu
ndi panu, kuyambira cipululu ndi Lebano, kuyambira nyanjayo,
nyanja ya Pirate, kufikira nyanja ya m'tsogolo, ndiwo malice
anu. 25Palibe munthu adzaima paraaso panu; Yehova Mulungu
wanu adzanjenjemeretsa ndi kuopsa dziko lonse mudzapondapo,
cifukwa ca inu, monga ananena ndi inu.

Mdalitso ndi temberero

26Taonani, ndirikuika pamaso panu lero dalitso ndi
temberero; 27dalitso, ngati mudzamvera malamulo a Yehova
Mulungu wanu amene ndikuuzani lero lino; 28koma temberero,
ngati simudzamvera malamulo a Yehova Mulungu wanu, ndi
kupatuka m'njira ndikuuzani lero lino, kutsata milungu yina imene
simunaidziwa.

29Ndipo kudzakhala, atakulowetsani Yehova Mulungu wanu m'dziko
limene mumkako kulilandira, munene mdalitso pa phiri la
Gerizimu, ndi temberero pa phiri la Ebala. 30Sakhala kodi tsidya lija
la Yordano, m'tseri mwace mwa njira yace yolowa dzuwa, m'dziko
la Akanani, akukhala m'cidikha, pandunji pace pa Giligala, pafupi
pa mathunda a More? 31Pakuti mulinkuoloka Yordano kulowa ndi
kulandira dziko limene Yehova Mulungu wanu akupatsani; ndipo
mudzacilandira colowa canu, ndi kukhalamo. 32Potero samalirani
kucita malemba ndi maweruzo onse ndiwaika pamaso panu lero
lino.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Malo Oyera akhale amodzi

1Awa ndi malemba ndi maweruzo, muziwasamalirawa kuwacita
m'dziko limene Yehova Mulungu wa makolo anu anakupatsani
likhale lanu lanu, masiku onse akukhala ndi moyo inu pa dziko
lapansi. 2Muononge konse malo onse, amitundu amene
mudzawalanda anatumikirako milungu yao, pa mapiri atali, ndi pa
zitunda, ndi pansi pa mitengo yonse yabiriwiri; 3nimugumule
maguwa ao a nsembe, ndi kuphwanya zoimiritsa zao, ndi kutentha
zifanizo zao, ndi kulikha mafano osema a milungu yao; ndipo
muononge dzina lao licoke m'malomo. 4Musamatero ndi Yehova
Mulungu wanu. 5Koma ku malo amene Yehova Mulungu wanu
adzasankha mwa mapfuko anu onse kuikapo dzina lace, ndiko ku
cokhalamo cace, muzifunako, ndi kufikako; 6ndi kubwera nazo
kumeneko nsembe zanu zopsereza, ndi nsembe zanu zophera, ndi
magawo anu onse a magawo khumi, ndi nsembe yokweza ya
dzanja lanu, ndi zowinda zanu, ndi nsembe zanu zaufulu, ndi
zoyamba kubadwa za ng'ombe zanu, ndi za nkhosa ndi mbuzi
zanu; 7ndipo kumeneko muzidya pamaso pa Yehova Mulungu
wanu, ndi kukondwera nazo zonse mudazigwira ndi dzanja lanu,
inu ndi a pa banja lanu, m'mene Yehova Mulungu wanu
anakudalitsani. 8Musamadzacita monga mwa zonse tizicita kuno
lero, yense kucita ciri conse ciyenera m'maso mwace; 9pakuti
mpaka lero simunafikira mpumulo ndi colowa, zimene Yehova
Mulungu wanu adzakupatsani. 10Koma mudzaoloka Yordano, ndi
kukhala m'dziko limene Yehova Mulungu wanu akulandiritsani;
ndipo adzakupumulitsani akulekeni adani anu onse pozungulirapo,
ndipo mudzakhala mokhazikika. 11Pamenepo padzakhala malo
amene Yehova Mulungu wanu adzasankha kukhalitsako dzina lace,
kumeneko muzibwera nazo zonse ndikuuzanizi; nsembe zanu
zopsereza, ndi nsembe zanu zophera, magawo anu onse a
magawo khumi, ndi nsembe yokweza dzanja lanu, ndi zowinda
zanu zosankhika zimene muzilonjezera Yehova. 12Ndipo
mudzakondwera pamaso pa Yehova Mulungu wanu, inu ndi ana
anu amuna, ndi ana anu akazi, ndi anchito anu amuna, ndi anchito
anu akazi, ndi Mlevi ali m'midzi mwanu, popeza alibe gawo kapena
colowa pamodzi ndi inu. 13Dzicenjerani nokha, musamapereka
nsembe zanu zopsereza pamalo ponse upaona: 14koma pamalo
pamene Yehova adzasankha, mwa limodzi la mapfuko anu,
pamenepo muzipereka nsembe zanu zopsereza, ndi pamenepo
muzicita zonse ndikuuzani. 15Koma monga mwa cikhumbu conse
ca moyo wanu muiphe ndi kudya nyama m'midzi yanu yonse,
monga mwa mdalitso wa Yehova Mulungu wanu anakupatsani;
odetsa ndi oyera adyeko, monga yamphoyo ndi yangondo. 16Mwazi

wao wokha musamadya; muziuthira panthaka ngati madzi. 17Simukhoza kudya m'mudzi mwanu limodzi la magawo khumi la tirigu wanu, kapena la vinyo wanu, kapena la mafuta anu, kapena oyambakubadwa a ng'ombe zanu kapena la nkhosa ndi mbuzi zanu, kapena zowinda zanu ziri zonse muzilonieza kapena nsembe zanu zaufulu, kapena nsembe yokweza ya m'dzanja lanu; 18koma muzizidya pamaso pa Yehova Mulungu wanu m'malo amene Yehova Mulungu wanu adzasankha, inu, ndi ana anu amuna, ndi ana anu akazi, ndi anchito anu amuna, ndi anchito anu akazi, ndi Mlevi ali m'mudzi mwanu; nimukondwere pamaso pa Yehova Mulungu wanu m'zonse mudazigwira ndi dzanja lanu. 19Dzicenjerani nokha, musataye Mlevi masiku onse akukhala inu m'dziko mwanu.

Za kudya nyama

20Akadzakuza malire a dziko lanu Yehova Mulungu wanu, monga ananena ndi inu, ndipo mukadzati, Ndidye nyama, popeza moyo wanga ukhumba kudya nyama; mudye nyama monga umo monse ukhumba moyo wanu. 21Malo amene Yehova Mulungu wanu adzasankha kuikako dzina lace akakutanimphirani, muziphako ng'ombe zanu ndi nkhosa ndi mbuzi zanu zimene Yehova anakupatsani, monga ndinakuuzani, ndi kuzidya m'mudzi mwanu, monga umo monse ukhumba moyo wanu. 22Koma monga umo amadya mphoyo ndi ngondo momwemo uzizidya; odetsa ndi oyera adyeko cimodzimodzi. 23Koma mulimbikepo ndi kusadya mwaziwo; popeza mwazi ndiwo moyo, nimusamadya moyo pamodzi ndi nyama yace. 24Musamadya uwu; muuthire pansi ngati madzi. 25Musamadya uwu; kuti cikukomereni inu, ndi ana anu akudza m'mbuyo mwanu, pakucita inu zoyenera pamaso pa Yehova. 26Zopatulika zanu zokha zimene muli nazo, ndi zowinda zanu, muzitenge, ndi kupita nazo ku malo amene Yehova adzasanka; 27ndipo mupereke nsembe zanu zopsereza, nyama zao ndi mwazi wao, pa guwa la nsembe la Yehova Mulungu wanu; ndipo athire mwazi wa nsembe zanu zophera pa guwa la nsembe la Yehova Mulungu wanu, koma nyama yace muidye. 28Samalirani ndi kumvera mau awa onse ndikuuzaniwa, kuti cikukomereni inu, ndi ana anu akudza m'mbuyo mwanu nthawi zonse, pocita inu zokoma ndi zoyenera pamaso pa Yehova Mulungu wanu.
29Pamene Yehova Mulungu wanu akadzadulatu amitundu pamaso panu, kumene mulowako kuwalandira, ndipo mutawalandira, ndi kukhala m'dziko lao, 30dzicenjerani nokha mungakodwe ndi kuwatsata, ataonongeka pamaso panu; ndi kuti mungafunsire milungu yao, ndi kuti, Amitundu awa atumikira milungu yao bwanji? ndicite momwemo inenso. 31Musamatero ndi Yehova Mulungu wanu; pakuti ziri zonse zinyansira Yehova, zimene azida

iye, iwowa anazicitira milungu yao; pakuti angakhale ana ao amuna ndi ana ao akazi awatentha m'moto, nsembe ya milungu yao.
32Ciri conse ndikuuzani, mucisamalire kucicita; musamaoniezako, kapena kucepsako.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Acenjere nao owanyenga kuwapembedzetsa mafano

1Akauka pakati pa inu mneneri, kapena wakulota maloto,
nakakupatsani cizindikilo kapena cozizwa; 2ndipo cizindikilo
kapena cozizwa adanenaci cifika, ndi kuti, Titsate milungu yina,
imene simunaidziwa, ndi kuitumikira; 3musamamvera mau a
mneneri uyu, kapena wolota maloto uyu; popeza Yehova Mulungu
wanu akuyesani, kuti adziwe ngati mukonda Yehova Mulungu wanu
ndi mtima wanu wonse, ndi moyo wanu wonse. 4Muziyenda
kutsata Yehova Mulungu wanu, ndi kumuopa, ndi kusunga
malamulo ace, ndi kumvera mau ace, ndi kumtumikira iye, ndi
kummamatira. 5Ndipo mneneriyo, kapena wolota malotoyo,
mumuphe; popeza ananena cosiyanitsa ndi Yehova Mulungu wanu,
amene anakuturutsani m'dziko la Aigupto, nakuombolani
m'nyumba ya akapolo; kuti akuceteni mutaye njira imene Yehova
Mulungu wanu anakulamulirani muziyendamo. Potero muzicotsa
coipaco pakati pa inu.
6Mbale wanu, ndiye mwana wa mai wanu, kapena mwana wanu
wamwamuna, kapena mwana wanu wamkazi, kapena mkazi wa
kumtima kwanu, kapena bwenzi lanu, ndiye ngati moyo wanu
wanu, akakukakamizani m'tseri, ndi kuti, Tipite titumikire milungu
yina, imene simunaidziwa, inu, kapena makolo anu; 7ndiyo
milungu ya mitundu ya anthu akuzungulira inu, akukhala pafupi
pali inu, kapena akukhala patali pali inu, kuyambira malekezero a
dziko lapansi kufikira malekezero ena a dziko
lapansi; 8musamabvomerezana naye, kapena kumvera iye; diso
lanu lisamcitire cifundo, kapena kumleka, kapena kumbisa; 9koma
muzimupha ndithu; liyambe dzanja lanu kukhala pa iye kumupha,
ndi pamenepo dzanja la anthu onse. 10Nimuzimponya miyala, kuti
afe; popeza anayesa kukucetani muleke Yehova Mulungu wanu,
amene anakuturutsani m'dziko la Aigupto, m'nyumba va
akapolo. 11Kuti Israyeli wonse amve, ndi kuopa, ndi kusaonieza
kucita coipa cotere conga ici pakati pa inu.
12Ukamva za umodzi wa midzi yanu, imene Yehova Mulungu wanu
akupatsani kukhalako, ndi kuti, 13Amuna ena opanda pace
anaturuka pakati pa inu, naceta okhala m'mudzi mwao, ndi kuti,
Timuke titumikire milungu yina, imene simunaidziwa; 14pamenepo
muzifunsira, ndi kulondola, ndi kufunsitsa; ndipo taonani, cikakhala
coona, catsimikizika cinthuci, kuti conyansa cotere cacitika pakati
pa inu; 15muzikanthatu okhala m'mudzi muja ndi lupanga
lakuthwa; ndi kuuononga konse, ndi zonse ziri m'mwemo, ng'ombe
zace zomwe, ndi lupanga lakuthwa. 16Ndipo muzikundika zofunkha
zace zonse pakati pakhwalala pace, nimutenthe ndi moto mudzi,
ndi zofunkha zace zonse konse, pamaso pa Yehova Mulungu wanu;

ndipo udzakhala mulu ku nthawi zonse; asaumangenso. 17Ndipo
pasamamatire padzanja panu kanthu ka cinthu coti cionongeke;
kuti Yehova a aleke mkwiyo wacewaukali, nakucitireni cifundo, ndi
kukumverani nsoni, ndi kukucurukitsani monga analumbirira
makolo anu; 18pakumvera inu mau a Yehova Mulungu wanu,
kusunga malamulo ace onse amene ndikuuzani lero lino, kucita
zoyenera pamaso pa Yehova Mulungu wanu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Za nyama yodyedwa ndi yosadyedwa

1Inu ndinu ana a Yehova Mulungu wanu; musamadziceka, kapena
kumeta tsitsi pakati pa maso cifukwa ca akufa. 2Popeza ndinu
mtundu wa anthu opatulikira Yehova Mulungu wanu, ndipo Yehova
anakusankhani mukhale mtundu wa anthu wa pa wokha wa iye
yekha, mwa mitundu yonse ya anthu okhala pankhope pa dziko
lapansi.
3Musamadya conyansa ciri conse, 4Nyamazi muyenera kumadya
ndi izi: ng'ombe, nkhosa, ndi mbuzi, 5ngondo, ndi nswala ndi
mphoyo, ndi mphalapala, ndi ngoma, ndi nyumbu, ndi
mbalale. 6Ndipo nyama iri yonse yogawanika ciboda, nikhala
yogawanikadi ciboda, nibzikula, imeneyo muyenera kudya. 7Koma
izi zokha simuyenera kuzidya mwa zobzikulazo, kapena
zogawanika ciboda: ngamila, ndi ka'ulu, ndi mbira,
popezazibzikula, komazosagawanika ciboda, muziyese
zodetsa; 8ndi nkhumba, popeza igawanika ciboda koma
yosabzikula, muiyese yodetsa; musamadya nyama yao,
musamakhudza mitembo yao.
9Mwa zonse ziri m'madzi muyenera kumadya izi: ziri zonse ziri
nazo zipsepse ndi mamba, zimenezi muyenera kumadya; 10koma
ziri zonse zopanda zipsepse kapena mamba musamadya;
muziyese zonyansa.
11Mbalame zosadetsazonse muyenera kumadya. 12Koma izi ndi
zimene simuyenera kumadya: mphungu, ndi nkhwazi, ndi
cikambi, 13ndi kamtema, ndi mphamba, ndi muimba monga mwa
mtundu wace; 14ndi khungubwe ali yense monga mwa mtundu
wace; 15ndi nthiwatiwa, ndi cipudo, ndi kakoa, ndi kabawi monga
mwa mtundu wace; 16ndi nkhutukutu, ndi mancici, ndi
tsekwe; 17ndi bvuwo, ndi dembu, ndi nswankhono; 18ndi iodwa, ndi
cimeza, monga mwa mtundu wace, ndi sadzu, ndi mleme. 19Ndipo
zokwawa zonse zakuuluka muziyesa zonyansa;
musamazidya. 20Mbalame zonse zosadetsa muyenera kumadya.
21Musamadya cinthu ciri conse citafa cokha; muzipereka ico kwa
mlendo ali m'mudzi mwanu, acidye ndiye; kapena ucigulitse kwa
mlendo; popeza ndinu mtundu wa anthu wopatulika wa Yehova
Mulungu wanu. Musamaphika mwana wa mbuzi mu mkaka wa
mace.

Za limodzi mwa magawo khumi

22Muzipereka ndithu limodzi la magawo khumi la zipatso zonse za
mbeu zanu, zofuma kumunda, caka ndi caka. 23Ndipo muzidye
pamaso pa Yehova Mulungu wanu, m'malo m'mene asankhamo
iye, kukhalitsamo dzina lace; limodzi la magawo khumi la tirigu
wanu, la vinyo wanu, ndi la mafuta anu, ndi oyamba kubadwa a

ng'ombe zanu ndi a nkhosa ndi mbuzi zanu; kuti muphunzire
kuopa Yehova Mulungu wanu masiku onse. 24Ndipo ikakutalikirani
njira kotero kuti simukhoza kulinyamula, popeza malo amene
Yehova Mulungu wanu adzasankha, kuikapo dzina lace,
akutanimphirani; atakudalitsani Yehova Mulungu
wanu; 25pamenepo mulisinthe ndarama, ndi kumanga ndarama
ikhale m'dzanja mwanu, ndi kupita ku malo amene Yehova
Mulungu wanu adzasankha; 26ndipo mugule ndi ndaramazo ciri
conse moyo wanu ukhumba, ng'ombe kapena nkhosa, kapena
vinyo, kapena cakumwa colimba, kapena ciri conse moyo wanu
ukufunsani; nimudye pomwepo pamaso pa Yehova Mulungu wanu,
ndi kukondwera, inu ndi a pabanja panu. 27Koma Mlevi wokhala
m'mudzi mwanu, musamamtaya, popeza alibe gawo kapena
colowa pamodzi ndi inu.
28Pakutha pace pa zaka zitatu muziturutsa magawo onse a
magawo khumi a zipatso zanu za caka ico, ndi kuwalinditsa
m'mudzi mwanu; 29ndipo abwere Mlevi, popeza alibe gawo kapena
colowa pamodzi ndi inu, ndi mlendo, ndi ana amasiye, ndi mkazi
wamasiye, okhala m'mudzi mwanu, nadye nakhute; kuti Yehova
Mulungu wanu akakudalitseni mu nchito zonse za dzanja lanu
muzicitazi.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Za caka ca cilekerero

1Pakutha Pace pa zaka zisanu ndi ziwiri pakhale
cilekerero. 2Cilekereroco ndici: okongoletsa onse alekerere
cokongoletsa mnansi wace; asacifunse kwa mnansi wace, kapena
mbale wace; popeza analalikira cilekerero ca Yehova. 3Muyenera
kucifunsa kwa mlendo; koma canu ciri conse ciri ndi mbale wanu,
dzanja lanu licilekerere; 4ndiko kuti pasakhale waumphawi mwa
inu; pakuti Yehova adzakudalitsani kwambiri m'dziko limene
Yehova Mulungu wanu akupatsani likhale colowa canu
canu; 5cokhaci mumvere cimverere mau a Yehova Mulungu wanu,
kuti musamalire kucita malamulo awa onse amene ndikuuzani lero
lino. 6Popeza Yehova Mulungu wanu adzakudalitsani, monza
ananena nanu; ndipo mudzakongoletsa amitundu ambiri,
osakongola nokha; nimudzacita ufumu pa amitundu ambiri, koma
iwo sadzacita ufumu pa inu.

Za aumphawi ndi aka polo

7Akakhala ndi inu munthu waumphawi, ndiye wilia wa abale anu,
m'umodzi wa midzi yanu, m'dziko limene Yehova Mulungu wanu
akupatsani, musakhakala mtima wanu, kapena kuumitsa dzanja
lanu kukaniza mbale wanu waumphawi; 8koma muzimtansira
dzanjalanundithu ndi kumkongoletsa ndithu zofikira kusowa kwace,
monga umo amasowa. 9Dzicenjerani, mungakhale mau opanda
pace mumtima mwanu, ndi kuti, Cayandika caka cacisanu ndi
ciwiri, caka ca cilekerero; ndipo diso lanu lingaipire mbale wanu
waumphawi, osampatsa kanthu; ndipo iye angalirire inu kwa
Yehova; ndipo mwa inu mungakhale cimo. 10Muzimpatsa ndithu,
osawawa mtima wanu pompatsa; popeza, cifukwa ca ici Yehova
Mulungu wanu adzakudalitsani mu nchito zanu zonse, ndi m'zonse
muikapo dzanja lanu. 11Popeza waumphawi salekana m'dziko,
cifukwa cace ndikuuzani ndi kuti, Dzanja lanu mulitansire ndithu
mbale wanu, ndi ozunzika anu, ndi aumphawi anu, a m'dziko
mwanu.
12Mukagula mbale wanu, Mhebri wamwamuna kapena Mhebri
wamkazi, ndipo adzakutumikira zaka zisanu ndi cimodzi; koma
caka cacisanu ndi ciwiri umlole acoke kwanu waufulu. 13Ndipo
pomlola iwe acoke kwanu waufulu, musamamlola acoke wopanda
kanthu; 14mumlemeze nazo za nkhosa ndi mbuzi zanu, ndi za
padwale, ndi za mosungira vinyo; monga Yehova Mulungu wanu
anakudalitsani mumninkhe uyu. 15Ndipo mukumbukile kuti munali
akapolo m'dziko la Aigupto, ndipo Yehova Mulungu wanu
anakuombolani; cifukwa cace ndikuuzani ici lero lino. 16Ndipo
kudzakhala, akanena ndi inu, Sindituruka kucoka kwanu; popeza
akonda inu ndi nyumba yanu, popeza kumkomera

kwanu; 17pamenepo muzitenga lisungulo, ndi kulipisa m'khutu
mwace, kulikanikiza ndi citseko, ndipo adzakhala kapolo wanu
kosalekeza. Muzicitanso momwemo ndi adzakazi
anu. 18Musamayesa neosautsa, pomlola akucokereni waufulu;
popeza anakugwirirani nchito zaka zisanu ndi cimodzi monga
wolipidwa wakulandira cowirikiza; potero Yehova Mulungu wanu
adzakudalitsani m'zonse muzicita.

Za nyama zoyamba kubadwa

19Zazimuna zonse zoyamba kubadwa, zobadwa mwa ng'ombe
zanu ndi mwa nkhosa ndi mbuzi zanu, muzizipatulira Yehova
Mulungu wanu; musamagwiritsa nchito yoyamba kubadwa mwa
ng'ombe zanu, kapena kusenga yoyamba kubadwa ya nkhosa
kapena mbuzi zanu. 20Muzidye caka ndi caka pamaso pa Yehova
Mulungu wanu, m'malo amene Yehova adzasankha, inu ndi a
m'banja mwanu. 21Koma ikakhala naco cirema, yotsimphina,
kapena yakhungu, cirema ciri conse coipa, musamaiphera nsembe
Yehova Mulungu wanu. 22Muidye m'mudzi mwanu; odetsa ndi
oyera aidye cimodzimodzi, monga mphoyo ndi nswala. 23Mwazi
wace wokha musamadya; muuthire pansi ngati madzi.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Madyerero a Paskha, a Masabata, ndi a Misasa

1Samalirani mwezi wa Abibu, kuti muzicitira Yehova Mulungu wanu
Paskha; popeza m'mwezi wa Abibu Yehova Mulungu wanu
anakuturutsani m'dziko la Aigupto usiku. 2Ndipo muziphera Yehova
Mulungu wanu nsembe ya Paskha, ya nkhosa ndi ya ng'ombe,
m'malo amene Yehova adzasankha kukhalitsamo dzina
lace. 3Musamadyera nayo mkaye wa cotupitsa; masiku asanu ndi
awiri mudyere nayo mkate wopanda cotupitsa, ndiwo mkate wa
cizunziko popeza munaturuka m'dziko la Aigupto mofulumira; kuti
inu kumbukile tsiku loturuka inu m'dziko la Aigupto masiku onse a
moyo wanu. 4Ndipo m'malire mwanu monse musaoneke cotupitsa
masiku asanu ndi awiri; nyama yomwe muiphere nsembe tsiku
loyamba madzulo, isatsaleko usiku wonse kufikira
m'mawa. 5Simuyenera kuphera nsembe ya Paskha m'midzi yanu iri
yonse, imene Yehova Mulungu wanu akupatsani; 6koma pamalo
pamene Yehova Mulungu wanu adzasankha kukhalitsapo dzina
lace, pamenepo muphere nsembe ya Paskha, madzulo, polowa
dzuwa, nyengo ya kuturuka inu m'Aigupto. 7Ndipo muiphike ndi
kuidya m'malo amene Yehova Mulungu wanu adzasankha; koma
m'mawa mwace mubwerere kumka ku mahema anu. 8Masiku
asanu ndi limodzi muzidya mkate wopanda cotupitsa; ndipo tsiku
lacisanu ndi ciwiri ndilo loletsa, la Yehova Mulungu wanu;
musamagwira nchito pamenepo.
9Mudziwerengere masabata asanu ndi awiri; muyambe kuwerenga
masabata asanu ndi awiri poyambira kuceka tirigu waciriri. 10Ndipo
mucitire Yehova Mulungu wanu madyerero a masabata, ndiwo
msonkho waufulu wa dzanja lanu, umene mupereke monga Yehova
Mulungu wanu akudalitsani. 11Ndipo mukondwere pamaso pa
Yehova Mulungu wanu, inu ndi ana anu amuna, ndi ana anu akazi,
ndi anchito anu amuna, ndi anchito anu akazi, ndi Mlevi wokhala
m'mudzi mwanu, ndi mlendo, ndi mwana wamasiye, ndi mkazi
wamasiye, okhala pakati pa inu, m'malo amene Yehova Mulungu
wanu adzasankha kukhalitsako dzina lace. 12Ndipo mukumbukire
kuti munali akapolo m'Aigupto; musamalire kucita malemba awa.
13Mudzicitire madyerero a misasa masiku asanu ndi awiri,
mutasunga za padwale ndi za mopondera
mphesa; 14nimukondwere m'madyerero mwanu, inu, ndi ana anu
amuna, ndi ana anu akazi, ndi anchito anu amuna, ndi anchito anu
akazi, ndi Mlevi, ndi mlendo, ndi mwana wamasiye, ndi mkazi
wamasiye okhala m'mudzi mwanu. 15Masiku asanu ndi awiri
mucitire Yehova Mulungu wanu madyerero m'malo amene Yehova
adzasankha; popeza Yehova Mulungu wanu adzakudalitsani
m'zipatso zanu zonse, ndi m'nchito zonse za manja anu;

nimukondwere monsemo. 16Amuna onse azioneka pamaso pa
Yehova Mulungu wanu m'malo amene iye adzasankha, katatu
m'caka; pa madyerero a mkate wopanda cotupitsa, pa madyerero
a masabata, ndi pa madyerero a misasa; ndipo asaoneke pamaso
pa Yehova opanda kanthu; 17apereke yense monga mwa mphatso
ya m'dzanja lace, monga mwa mdalitso wa Yehova Mulungu wanu
anakupatsani.

Za oweruza mirandu

18Mudziikire oweruza ndi akapitao m'inidzi yanu yonse imene
Yehova Mulungu wanu akupatsani, monga mwa mapfuko anu;
ndipo aweruze anthu ndi ciweruzo colungama. 19Musamapotoza
ciweruzo, musamasamalira munthu, kapena kulandira
cokometsera mlandu; popeza cokometsera mlandu cidetsa maso a
anzeru, niciipsa mau a olungama. 20Cilungamo, cilungamo ndico
muzicitsata, kuti mukhale ndi moyo ndi kulandira dziko limene
Yehova Mulungu wanu akupatsani.
21Musamadziokera mitengo iri yonse ikhale nkhalango pafupi pa
guwa la nsembe la Yehova Mulungu wanu, limene
mwadzimangira. 22Ndipo musamadziutsira coimiritsa ciri conse
cimene Yehova Mulungu wanu adana naco.

©The Bible Society of Malawi, 1992

1Musamaphera Yehova Mulungu wanu nsembe ya ng'ombe, kapena
nkhosa, yokhala naco cirema, kapena ciri conse coipa; pakuti
cinyansira Yehova Mulungu wanu. 2Akapeza pakati panu, m'mudzi
wanu wina umene anakupatsani Yehova Mulungu wanu,
wamwamuna kapena wamkazi wakucita ciri coipa pamaso pa
Yehova Mulungu wanu, ndi kulakwira cipangano cace, 3nakatumikira
milungu yina, naigwadira iyo, kapena dzuwa, kapena mwezi,
kapena wina wa khamu la kuthambo, losauza Ine; 4ndipo
akakuuzani, nimudamva, pamenepo muzifunsitsa, ndipo taonani,
cikakhala coonadi, coti nzenizeni, conyansaci cacitika
m'Israyeli; 5pamenepo muturutse mwamunayo kapena mkaziyo,
anacita coipaco, kumka naye ku zipata zanu, ndiye wamwamuna
kapena wamkazi; ndipo muwaponye miyala, kuti afe. 6Pakamwa pa
mboni ziwiri kapena zitatu amuphe iye amene akuti afe; asamuphe
pakamwa pa mboni imodzi. 7Liyambe kumgwera dzanja la mboniyo
kumupha; pamenepo dzanja la anthu onse, Potero muzicotsa
coipaco pakati panu.
8Ukakulakani mlandu pouweruza, ndiwo wakunena zamwazi,
kapena zakutsutsana, kapena zakupandana, ndiyo mirandu
yakutengana m'midzi mwanu; pamenepo muziuka ndi kukwera
kumka ku malo amene Yehova Mulungu wanu
adzasankha; 9nimufike kwa ansembe, Alevi, ndi kwa woweruza wa
m'masiku awo; nimufunsire; ndipo adzakufotokozerani
maweruzidwe ace. 10Ndipo mucite monga momwe ananena mau
akufotokozeraniwo, ku malo amene Yehova adzawasankha;
nimusamalire kucita monga mwa zonse akulangizanizi, 11Monga
momwe anena malamulo akulangizani, ndi monga mwa ciweruzo
akufotokozerani, mucite; mau akufotokozerani musawapatukire
kulamanja kapena kulamanzere. 12Koma munthu wakucita
modzikuza, osamvera wansembe wokhala ciriri kutumikirako
pamaso pa Yehova Mulungu wanu, kapena woweruza, munthuyo
afe; ndipo mucotse coipaco kwa Israyeli. 13Ndipo anthu onse
adzamva ndi kucita mantha, osacitanso modzikuza.

Za kusankha mfumu ndi zomuyenera

14Mutakalowa m'dziko limene Yehova Mulungu wanu akupatsani,
ndi kulilandira lanu lanu, ndi kukhalamo; ndipo mukanena,
Tidziikire mfumu, monga amitundu onse akutizinga; 15mumuiketu
mfumu yanu imene Yehova Mulungu wanu adzaisankha; wina
pakati pa abale anu mumuike mfumu yanu; simuyenera kudziikira
mlendo, wosakhala mbale wanu. 16Koma asadzicurukitsire akavalo
iye, kapena kubwereretsa anthu amke ku Aigupto, kuti acurukitse
akavalo; popeza Yehova anati nanu, Musamabwereranso njira
iyi. 17Ndipo asadzicurukitsire akazi, kuti ungapatuke mtinta wace;

kapena asadzicurukitsire kwambiri siliva ndi golidi. 18Ndipo kudzali,
pakukhala iye pa mpando wacifumu wa ufumu wace,
adzilemberere cofanana ca cilamuloici m'buku, acitenge pa ici ciri
pamaso pa ansembe Alevi; 19ndipo azikhala naco, nawerengemo
masiku onse a moyo wace; kuti aphunzire kuopa Yehova Mulungu
wace, kusunga mau ons acilamulo ici ndi malemba awa,
kuwacita; 20kuti mtima wace usadzikuze pa abaleace, ndi kuti
asapatukire lamulolo, kulamanja kapena kulamanzere; kuti acuruke
masiku ace, m'ufumu wace, iye ndi ana ace pakati pa Israyeli.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Zoyenera ansembe ndi Alevi

1Ansembe Alevi, pfuko lonse la Levi, alibe gawo kapena colowa
pamodzi ndi Israyeli; azizidya nsembe zamoto za Yehova, ndi
colowa cace, 2Alibe colowa pakati pa abale ao; Yehova mwini wace
ndiye colowa cao, monga ananena nao. 3Ndipo zoyenera ansembe,
awapatse anthu akuphera nsembe ndizo: ingakhale ng'ombe
kapena nkhosa azipatsa wansembe mwendo wamwamba, ndi ya
m'masaya ndi chipfu. 4Zipatso zoyamba za tirigu wanu, za vinyo
wanu, ndi za mafuta anu ndi ubweya woyamba kuusenga,
muwapatse izi. 5Popeza Yehova Mulungu wanu anawasankha mwa
mapfuko anu onse, aimirire natumikire m'dzina la Yehova, iwo ndi
ana ao amuna kosalekeza.
6Ndipo Mlevi akacokera ku mudzi wanu wina m'Israyeli monse,
kumene akhalako, nakadza ndi cifuniro conse ca moyo wace ku
malo amene Yehova adzasankha; 7pamenepo azitumikira m'dzina
la Yehova Mulungu wace, monga amacita abale ace onse Alevi
akuimirirako pamaso pa Yehova. 8Cakudya cao cizifanana,
osawerengapo zolowa zace zogulitsa.

Mulungu aipidwa nao anyanga nil; obwebweta ndi onse otere

9Mutakalowa m'dziko limene Yehova Mulungu wanu akupatsani,
musamaphunzira kucita mongamwa zonyansa za amitundu
aja. 10Asapezeke mwa inu munthu wakupitiriza mwana wace
wamwamuna kapena mwana wace wamkazi ku mota wa ula,
wosamalira mitambo, kapena wosamalira kulira kwa mbalame,
kapena wanyanga. 11Kapena wotsirika, kapena wobwebweta,
kapena wopenduza, kapena wofunsira akufa. 12Popeza ali yense
wakucita izi Yehova anyansidwa naye; ndipo cifukwa ca zonyansa
izi Yehova Mulungu wanu awapitikitsa pamaso panu. 13Mukhale
angwiro ndi Yehova Mulungu wanu. 14Pakuti amitundu awa amene
mudzawalandira, amamvera iwo akuyesa mitambo, ndi a ula;
koma inu, Yehova Mulungu wanu sakulolani kucita cotero.

Lonjezo lakuti adzabadwa Mneneri womveka

15Yehova Mulungu wanu adzakuukitsirani mneneri wa pakati panu,
wa abale anu, wonga ine; muzimvera iye; 16monga mwa zonse
munafunsa Yehova Mulungu wanu m'Horebe, tsiku lakusonkhana
lija, ndi kuti, Tisamvenso mau a Yehova Mulungu wathu, ndipo
tisaonenso mota waukuru uwu, kuti tingafe. 17Ndipo Yehova anati
kwa ine, Cokoma ananenaci. 18Ndidzawaukitsira mneneri wa pakati
pa abale ao, wonga iwe; ndipo ndidzampatsa mau anga m'kamwa
mwace, ndipo adzanena nao zonse ndimuuzazi. 19Ndipo
kudzakhala kuti munthu wosamvera mau anga amene amanena
m'dzina langa, ndidzamfunsa. 20Koma mneneri wakucita

modzikuza ndi kunena mau m'dzina langa, amene
sindinamlamulira anene, kapena kunena m'dzina la milungu yina,
mneneri ameneyo afe. 21Ndipo mukati m'mtima mwanu,
Tidzazindikira bwanji mau amene Yehova sananena? 22Mneneri
akanena m'dzina la Yehova, koma mau adanenawa sacitika,
nisafika, ndiwo mau Yehova sanawanena; mneneriyo ananena
modzikuza, musamuopa iye.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Za midzi yopulumukirako

1Pamene Yehova Mulungu wanu ataononga amitundu, amene
Yehova Mulungu wanu akupatsani dziko lao, ndipo mutalilandira
lanu lanu, ndi kukhala m'midzi mwao, ndi m'nyumba
zao; 2pamenepo mudzipatulire midzi itatu pakati pa dziko lanu,
limene Yehova Mulungu wanu akupatsani likhale lanu
lanu. 3Mudzikonzere njira, ndi kugawa malire a dziko lanu, limene
Yehova Mulungu wanu akupatsani likhale lanu lanu, patatu; kuti
wakupha munthu athawireko. 4Ndipo mlandu wa munthu wakupha
mnzace wakuthawirako nakhala ndi moyo ndiwo: wakupha mnzace
osati dala, osamuda kale lonse; 5monga ngati munthu analowa
kunkhalango ndi mnzace kutema mitengo, ndi dzanja lace
liyendetsa nkhwangwa kutema mtengo, ndi nkhwangwa iguruka
m'mpinimo, nikomana ndi mnzace, nafa nayo; athawire ku wina wa
midzi iyi, kuti akhale ndi moyo; 6kuti wolipsa mwazi angalondole
wakupha mnzace, pokhala mtima wace watentha, nampeza,
popeza njira njaitali, namkantha kuti wafa; angakhale
sanaparamula imfa, poona sanamuda kale lonse. 7Cifukwa cace
ndikuuzani ndi kuti, Mudzipatulire midzi itatu. 8Ndipo Yehova
Mulungu wanu akakulitsa malire anu, monga analumbirira makolo
anu, ndi kukupatsani dziko lonse limene ananena kwa makolo anu
kuwapatsa ili; 9ukadzasunga lamulo ili lonse kulicita, limene
ndikuuzani lero lino, kukonda Yehova Mulungu wanu, ndi kuyenda
m'njira zace masiku onse; pamenepo mudzionjezere midzi itatu
yina pamodzi ndi itatu iyi; 10kuti angakhetse mwazi wosacimwa
pakati pa dziko lanu, limene Yehova Mulungu wanu akupatsani
likhale colowa canu, pangakhale mwazi pa inu. 11Koma munthu
akamuda mnzace, namlalira, ndi kumuukira ndi kumkanth a moyo
wace, kuti wafa; nakathawira ku wina wa midzi iyi; 12pamenepo
akuru a mudzi wace atumize ndi kumtengako ndi kumpereka
m'manja mwa wolipsa mwazi, kuti afe. 13Diso lanu lisamcitire
cifundo, koma mucotse mwazi wosacimwa m'Israyeli, kuti
cikukomereni.

Za kusendeza malire, ndi za mboni yonama

14Musamasendeza malire a mnansi wanu, amene adawaika iwo a
kale lomwe, m'colowa canu mudzalandiraci, m'dziko limene Yehova
Mulungu wanu akupatsani likhale lanu lanu.
15Mboni imodzi isamaukira munthu pa mphulupulu iri yonse,
kapena cimo liri lonse adalicimwa; pakamwa pa mboni ziwiri,
kapena pakamwa pa mboni zitatu mlandu utsimikizike. 16Mboni
yaciwawa ikaukira munthu kumneneza ndi kuti
analakwa; 17pamenepo anthu onse awiri, pakati pao pali
makaniwo, aziima pamaso pa Yehova, pamaso pa ansembe ndi

oweruza okhala m'masiku awa; 18ndipo oweruza afunsitse bwino;
ndipo taonani, mboniyo ikakhala mboni yonama, yomnamizira
mbale wace; 19mumcitire monga iye anayesa kumcitira mbale
wace; motero mucotse coipaco pakati panu. 20Ndipo otsalawo
adzamva, nadzaopa, ndi kusacitanso monga coipaco pakati
panu. 21Ndipo diso lanu lisacite cifundo, moyo kulipa moyo, diso
kulipa diso, dzino kulipa dzino, dzanja kulipa dzanja, phazi kulipa
phazi.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Malamulo a kunkhondo

1Pamene muturuka pa mdani wanu kunkhondo, ndi kuona akavalo
ndi magareta ndi anthu akucurukira inu, musawaopa; popeza
Yehova Mulungu wanu, amene anakukwezani kukuturutsani
m'dziko la Aigupto, ali ndi inu. 2Ndipo kudzali, pamene
muyandikiza kunkhondo, ayandikize wansembe nanene ndi
anthu, 3nati nao, Tamverani, Israyeli, muyandikiza kunkhondo lero
paadani anu; musalumuka mitima yanu; musacita mantha, kapena
kunjenjemera, kapena kuopsedwa pamaso pao; 4pakuti Yehova
Mulungu wanu ndiye wakumuka nanu, kugwirira inu pa adani anu,
kukupulumutsani. 5Ndipo akapitao anene ndi anthu, ndi kuti, Ndani
munthuyo anamanga nyumba yatsopano, osalowamo? amuke
nabwerere kunyumba kwace, kuti angafe kunkhondo nangalowemo
munthu wina. 6Ndipo ndani munthuyo ananka munda wamphesa
osalawa zipatso zace? amuke nabwerere ku nyumba yace, kuti
angafe kunkhondo, nangalawe munthu wina zipatso zace. 7Ndipo
munthuyo ndani anapala bwenzi ndi mkazi osamtenga? amuke
nabwerere kunyumba kwace, kuti angafe kunkhondo,
nangamtenge munthu wina. 8Pamenepo akapitao anenenso kwa
anthu, ndi kuti, Munthuyo ndani wakucita mantha ndi wofumuka
mtima? amuke nabwerere kunyumba kwace, ingasungunuke
mitima ya abale ace monga mtima wace. 9Ndipo kudzali, atatha
akapitao kunena ndi anthu, aike akazembe a makamu atsogolere
anthu.
10Pamene muyandikiza mudzi kucita nao nkhondo, muziupfuulira
ndi mtendere. 11Ndipo kudzali, ukakubwezerani mau a mtendere,
ndi kukutsegulirani, pamenepo anthu onse opereka m'mwemo
akhale alambi anu, nadzakutumikirani. 12Koma ukapanda kucita
zamtendere ndi inu, koma kucita nkhondo nanu, pamenepo
uumangire tsasa. 13Ndipo pamene Yehova Mulungu wanu aupereka
m'dzanja lanu, mukanthe amuna ace onse ndi lupanga
lakuthwa. 14Koma akazi ndi ana ndi ng'ombe ndi zonse ziti
m'mudzimo, zankhondo zace zonse, mudzifunkhire nokha; ndipo
mudye zankhondo za adani anu, zimene Yehova Mulungu wanu
anakupatsani. 15Muzitero nayo midzi yonse yokhala kutaritari ndi
inu, yosakhala midzi ya amitundu awa. 16Koma za midzi ya
amitundu awa, imene Yehova Mulungu wanu akupatsani, ikhale
colowa canu, musasiyepo camoyo ciri conse cakupuma; 17koma
muwaononge konse Ahiti, ndi Aamori, Akanani, ndi Aperizi, Ahivi
ndi Ayebusi; monga Yehova Mulungu wanu anakulamulirani; 18kuti
angakuphunzitseni kucita monga mwa zonyansa zao zonse,
amazicitira milungu yao; ndipo mungacimwire Yehova Mulungu
wanu.

19Pamene mumangira tsasa mudzi masiku ambiri, pouthirira
nkhondo kuugwira, usamaononga mitengo yace ndi kuitema ndi
nkhwangwa; pakuti ukadyeko, osailikha; pakuti mtengo wa
m'munda ndiwo munthu kodi kuti uumangire tsasa? 20Koma
mitengo yoidziwa inu kuti si ndiyo mitengo yazipatso, imeneyi
muiononge ndi kuilikha; ndipo mudzi wocita nanu nkhondo
muumangire macemba, mpaka mukaugonjetsa.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Za wophedwa mosadziwika

1Akapeza munthu waphedwa m'dziko limene Yehova Mulungu
wanu akupatsani likhale lanu lanu, nagona pamunda, wosadziwika
wakumkantha, 2pamenepo azituruka akuru anu ndi oweruza anu,
nayese ku midzi yomzinga wophedwayo; 3ndipo kudzali kuti mudzi
wakukhala kufupi kwa munthu wophedwayo, inde akuru a mudzi
uwu atenge ng'ombe yamsoti yosagwira nchito, yosakoka
goli; 4ndipo akuru a mudzi uwu atsike nao msotiwo ku cigwa
coyendako madzi, cosalima ndi cosabzala, naudula khosi msotiwo
m'cigwamo; 5ndipo ansembe, ana a Levi, ayandikize; pakuti
Yehova Mulungu wanu anasankha iwo kumtumikira ndi kudalitsa
m'dzina la Yehova; ndipo kutengana konse ndi kupandana konse
kukonzeke monga mwa mau awa. 6Ndipo akuru onse a mudziwo
wokhala pafupi pa munthu wophedwayo azisamba manja ao pa
msoti woudula khosi m'cigwamo; 7nayankhe nati, Manja athu
sanakhetsa mwazi uwu, ndi maso athu sanauona. 8Landirani,
Yehova, cotetezera anthu anu Israyeli, amene munawaombola,
ndipo musalole mwazi wosacimwa ukhale pakati pa anthu anu
Israyeli; ndipo adzawatetezera ca mwaziwo. 9Cotero mudzicotsere
mwazi wosacimwa pakati panu, pakuti wacita coyenera pamaso pa
Yehova.

Za akazi otengedwa kunkhondo

10Pamene muturuka kumka ku nkhondo ya pa adani anu, ndipo
Yehova Mulungu wanu awapereka m'manja mwanu, ndipo
muwagwira akhale akapolo anu; 11mukaona mwa akapolowa mkazi
wokongola, mukamkhumba, ndi kufuna kumtenga akhale mkazi
wanu; 12pamenepo mufike naye kwanu ku nyumba yanu; ndipo
amete tsitsi la pamutu pace, ndi kuwenga makadabo
ace; 13nabvule zobvala za ukapolo wace, nakhale m'nyumba
mwanu, nalire atate wace, ndi mai wace mwezi wamphumphu;
ndipo atatero mulowe naye ndi kukhala mwamuna wace, ndi iye
akhale mkazi wanu. 14Ndipo kudzali, mukapanda kukondwera
naye, mumlole apite komwe afuna; koma musamgulitsa ndalama
konse, musamamuyesa cuma, popeza wamcepetsa.

Mphamvu ya oyamba kubadwa

15Munthu akakhala nao akazi awiri, wina wokondana naye, wina
wodana naye, nakambalira ana, wokondana naye, ndi wodana
naye yemwe; ndipo mwana wamwamuna woyamba akakhala wa
iye uja anadana naye; 16pamenepo kudzali, tsiku lakugawira ana
ace amuna cuma cace, sangakhoze kuyesa mwana wa wokondana
naye woyamba kubadwa, wosati mwana wa wodana naye, ndiye
woyamba kubadwatu. 17Koma azibvomereza wobadwa woyamba,
mwana wa wodana naye, ndi kumwirikizira gawo lace la zace

zonse; popeza iye ndiye ciyambi ca mphamvu yace; zoyenera
woyamba kubadwa nzace.

Za ana opulukira osamvera

18Munthu akakhala naye mwana wamwamuna wopulukira, ndi
wopikisana naye, wosamvera mau a atate wace, kapena mau a
mai wace, wosawamvera angakhale anamlanga; 19azimgwira atate
wace ndi mai wace, ndi kuturukira naye kwa akuru a mudzi wace,
ndi ku cipata ca malo ace; 20ndipo anene kwa akulu a mudzi wace,
Mwana wathu wamwamuna uyu ngwopulukira ndi wopikisana nafe,
wosamvera mau athu, ndiye womwazamwaza, ndi
woledzera. 21Pamenepo amuna onse a mudzi wace amponye
miyala kuti afe; cotero mucotse coipaco pakati panu; ndipo Israyeli
wonse adzamva, nadzaopa.

Za kuika wophedwa mompacika

22Munthu akakhala nalo cimo loyenera imfa, kuti amuphe, ndipo
wampacika; 23mtembo wace usakhale pamtengo usiku wonse,
koma mumuike ndithu tsiku lomwelo; pakuti wopacikidwa
pamtengo atembereredwa ndi Mulungu; kuti mungadetse dziko
lanu limene Yehova Mulungu wanu akupatsani likhale colowa canu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Za zoweta zolowerera

1Mukapenya ng'ombe kapena nkhosa ya mbale wako zirikusokera
musamazilekerera, muzimbwezera mbale wanu ndithu. 2Ndipo
ngati mbale wanu sakhala pafupi ndi inu, kapena mukapanda
kumdziwa, mubwere nayo kwanu ku nyumba yanu, kuti ikhale
kwanu, kufikira mbale wanu akaifuna, ndipo wambwezera
iyo. 3Mutero nayenso buru wace; mutero naconso cobvala cace;
mutero naconso cotayika ciri conse ca mbale wanu, cakumtayikira
mukacipeza ndi inu; musamazilekerera. 4Mukapenya buru kapena
ng'ombe ya mbale wanu, zitagwa m'njira, musamazilekerera;
mumthandize ndithu kuziutsanso.

Zosayenerana zisaphatikizike

5Mkazi asabvale cobvala ca mwa muna, kapena mwamuna
asabvale cobvala ca mkazi; pakuti ali yense wakucita izi Yehova
Mulungu wanu anyansidwa naye.
6Mukacipeza cisa ca mbalame panjira, mumtengo kapena
panthaka pansi, muli ana kapena mazira, ndi mace alikuumatira
ana kapena mazira, musamatenga mace pamodzi ndi
ana; 7muloletu mace amuke, koma mudzitengere ana; kuti
cikukomereni, ndi kuti masiku anu acuruke.
8Pamene mumanga nyumba yatsopano, muzimanga kampanda pa
tsindwi lace, kuti ungatengere nyumba yanu mwazi, akagwako
munthu. 9Musamabzala mbeu zosiyana m'munda wanu
wamphesa, kuti zingaipsidwe mbeu zonse udazibzala, ndi zipatso
za munda wamphesa zomwe.
10Musamalima ndi buru ndi ng'ombe zikoke
pamodzi. 11Musamabvala nsaru yosokonezeka yaubweya pamodzi
ndi thonje.
12Mudzipangire mphonje pa ngondya zinai za copfunda canu
cimene mudzipfunda naco.

Za akazi onenezedwa

13Munthu akatenga mkazi, nalowana naye, namuda, 14namneneza
zoutsa mbiri yamanyazi, ndi kumveketsa dzina loipa, ndi kuti,
Ndinamtenga mkazi uyu, koma polowana nave sindinapeza
zizindikilo zakuti ndiye namwali ndithu; 15pamenepo atate wa
namwaliyo ndi mai wace azitenga ndi kuturuka nazo zizindikilo za
unamwali wace wa namwaliyo, kumka nazo kwa akuru a mudzi
kucipata; 16ndipo atate wa namwaliyo azinena kwa akuru,
Ndinampatsa munthuyu mwana wanga wamkazi akhale mkazi
wace, koma amuda; 17ndipo, taonani, wamneneza zoutsa mbiri
yamanyazi, ndi kuti, Sindinapeza zizindikilo za unamwali wace
in'mwana wako wamkazi; koma si izi zizindikilo za unamwali wa
mwana wanga wamkazi. Ndipo azifunyulula cobvalaco pamaso pa

akulu a mudziwo. 18Pamenepo akuru a mudziwo azitenga
munthuyu ndi kumkwapula; 19ndi kumlipitsa masekeli makumi
okha okha khumi a siliva, ndi kuipereka kwa atate wa namwaliyo,
popeza anamveketsa dzina loipa namwali wa Israyeli, ndipo
azikhala mkazi wace, sakhoza kumcotsa masiku ace onse. 20Koma
cikakhala coona ici, kuti zizindikilo zakuti ndiye namwali
zidamsowa namwaliyo; 21pamenepo azimturutsa namwaliyo ku
khomo la nyumba ya atate wace, ndipo amuna a mudzi wace
azimponya miyala kuti afe; popeza anacita copusa m'Israyeli,
kucita cigololo m'nyumba ya atate wace; cotero uzicotsa coipaco
pakati panu.

Zoyanjana zosaloledwa

22Akampeza munthu alikugona ndi mkazi wokwatibwa ndi
mwamuna; afe onse awiri, mwamuna wakugona ndi mkazi, ndi
mkazi yemwe; cotero muzicotsa coipaco mwa Israyeli.
23Pakakhala namwali, wosadziwa mwamuna, wopalidwa ubwenzi
ndi mwamuna, ndipo anampeza m'mudzi mwamuna, nagona
nave; 24muziwaturutsa onse awiri kumka nao ku cipata ca mudzi
uwo, ndi kuwaponya miyala kuti afe; namwaliyo popeza sanapfuula
angakhale anali m'mudzi; ndi mwamuna popeza anacepetsa mkazi
wa mnansi wace; cotero muzicotsa coipaco pakati panu.
25Koma mwamuna akapeza namwali wopalidwa bwenzi kuthengo,
namgwira mwamunayo, nagona naye; pamenepo afe mwamuna
yekha wogona naye; 26koma namwaliyo musamamcitira kanthu;
namwaliyo alibe cimo loyenera imfa; pakuti mlandu uwu ukunga
munthu waukira mnzace namupha; 27pakuti anampeza kuthengo;
namwali wopalidwa bwenziyo anapfuula, koma panalibe
wompulumutsa.
28Munthu akapeza namwali wosadziwa mwamuna, ndiye
wosapalidwa ubwenzi, oakamgwira nagona naye, napezedwa
iwo, 29pamenepo mwamuna amene anagona naye azipatsa atate
wace wa namwaliyo masekeli makumi asanu a siliva, ndipo
azikhala mkazi wace; popeza anamcepetsa; sakhoza kumcotsa
masiku ace onse.
30Munthu asatenge mkazi wa atate wace, kapena kubvula atate
wace.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Oletsedwa ku msonkhano wa Yehova

1Munthu wophwetekwa, wophwanyika kapena wofulika, asalowe
m'msonkhano wa Yehova.
2Mwana wa m'cigololo asalowe m'msonkhano wa Yehova, ngakhale
mbadwo wace wakhumi usalowe m'msonkhano wa Yehova.
3M-amoni kapena Mmoabu asalowe m'msonkhano wa Yehova;
ngakhale mbadwo wao wakhumi usalowe m'msonkhano wa
Yehova, ku nthawi zonse; 4popeza sanakukumikani ndi mkate ndi
madzi m'njira muja munaturuka m'Aigupto; popezanso
anakulembererani Balamu mwana wa Beori wa ku Petori wa
Mesapotamiya, kuti akutembererereni. 5Ndipo Yehova Mulungu wanu
sanafuna kumvera Balamu; koma Yehova Mulungu wanu
anakusandulizirani tembererolo likhale mdalitso, popeza Yehova
Mulungu wanu anakukondani. 6Musawafunira mtendere, kapena
cowakomera masiku anu onse ku nthawi zonse.
7Musamanyansidwa naye M-edomu, popeza ndiye mbale wanu;
musamanyansidwa naye M-aigupto, popeza munali alendo m'dziko
lace. 8Ana obadwa nao a mbadwo wacitatu alowe m'msonkhano
wa Yehova. 9Nkhondo yanu ikaturuka pa adani anu, mudzisunge
kusacita coipa ciri conse. 10Pakakhala munthu pakati pa inu, ndiye
wosayera cifukwa cocitika usiku, azituruka kunja kwa cigono,
asalowe pakati pa cigono; 11koma kudzali pofika madzulo, asambe
m'madzi; ndipo litalowa dzuwa alowe pakati pa cigono. 12Mukhale
nao malo kunja kwa cigono kumene muzimukako
kuthengo; 13nimukhale naco cokumbira mwa zida zanu; ndipo
kudzali, pakukhala inu pansi kuthengo mukumbe naco, ndi
kutembenuka ndi kufotsera cakuturukaco; 14popeza Yehova
Mulungu wanu ayenda pakati pa cigono canu, kukupulumutsani ndi
kupereka adani anu pamaso panu; cifukwa cace cigono canu
cikhale copatulika; kuti angaone kanthu kodetsa mwa inu, ndi
kukupotolokerani.

Za akapolo opulumuka, za acigololo, za okongoletsa mopindulitsa

15Musamapereka kwa mbuye wace kapolo wopulumuka kwa
mbuye wace kuthawira kwa inu; 16akhale nanu, pakati panu, ku
malo asankhako iye m'mudzi mwanu mwina momkonda;
musamamsautsa.
17Pasakhale mkazi wacigololo pakati pa ana akazi a Israyeli,
kapena wacigololo pakati pa ana amuna a
Israyeli. 18Musamabwera nayo mphotho ya wacigololo, kapena
mtengo wace wa garu kulowa nazo m'nyumba ya Yehova Mulungu
wanu, cifukwa ca cowinda ciri conse; pakuti onse awiriwa Yehova
Mulungu wanu anyansidwa nao.

19Musamakongoletsa mbale wanu mopindulitsa; phindu la
ndarama, phindu la cakudya, phindu la kanthu kali konse
kokongoletsa. 20Mukongoletse mlendo mopindulitsa; koma mbale
wanu musamamkongoletsa mopindulitsa, kuti Yehova Mulungu
wanu akudalitseni mwa zonse muzigwira ndi dzanja lanu, m'dziko
limene mulowamo kulilandira.
21Mukawindira Yehova Mulungu wanu cowinda, musamacedwa
kucicita; popeza Yehova Mulungu wanu adzakufunsani za ici ndithu
ndipo mukadacimwako. 22Koma mukapanda kulonieza cowinda,
mulibe kucimwa. 23Coturuka pa milomo yanu mucisamalire ndi
kucicita; monga munaloniezera Yehova Mulungu wanu, copereka
caufulu munacilonjeza pakamwa panu.
24Mukalowa m'munda wamphesa wa mnansi wanu, mudyeko
mphesa ndi kukhuta nazo monga mufuna eni koma musaika
kanthu m'cotengera canu.
25Mukalowa m'tirigu wosasenga wa mnansi wanu, mubudule ngala
ndi dzanja lanu, koma musasengako ndi zenga tirigu waciriri wa
mnansi wanu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Za kalata wa cilekaniro, cikole, kuba munthu, khate

1Munthu akatenga mkazi akhale wace, kudzali, ngati sapeza ufulu
pamaso pace, popeza anapeza mwa iye kanthu kosayenera,
amlembere kalata wa cilekanitso, ndi kumpereka uyu m'dzanja
lace, ndi kumturutsa m'nyumba mwace. 2Ndipo ataturuka
m'nyumba mwace, amuke nakhale mkazi wa mwamuna
wina. 3Ndipo akamuda mwamuna waciwiriyo, nakamlemberanso
kalata wa cilekanitso, ndi kumpereka uyu m'dzanja lace,
nakamturutsa m'nyumba mwace; kapena akamwalira mwamuna
wotsirizayo, amene anamtenga akhale mkazi wace; 4pamenepo
mwamuna woyamba anamcotsayo sangathe kumtenganso akhale
mkazi wace, atadetsedwa iye; pakuti ici ndi conyansa pamaso pa
Yehova; ndipo usamacimwitsa dziko, limene Yehova Mulungu wanu
akupatsani likhale colandira canu.
5Munthu akatenga mkazi watsopano, asaturuke nayo nkhondo,
kapena asamcititse kanthu kali konse; akhale waufulu ku nyumba
yace caka cimodzi, nakondweretse mkazi adamtengayo. 6Munthu
asalandire cikole mphero, ngakhale mwanamphero, popeza
alandirapo cikole moyo wamunthu.
7Akampeza munthu waba mbale wace wina wa ana a Israyeli,
namuyesa kapolo, kapena wamgulitsa, afe wakubayo; potero
muzicotsa coipaco pakati panu.
8Cenjerani nayo nthenda yakhate, kusamaliratu, ndi kucita monga
mwa zonse akuphunzitsani ansembe Alevi; monga ndinalamulira
iwo, momwemo muzisamalira kucita. 9Kumbukilani cimene Yehova
Mulungu wanu anacitira Miriamu panjira, poturuka inu m'dziko la
Aigupto.

Za kukongoletsa

10Mukakongoletsa mnansi wanu ngongole iri yonse, musamalowa
m'nyumba mwace kudzitengera cikole cace. 11Muime pabwalo, ndi
munthu amene umkongoletsayo azituruka naco cikoleco kwa inu
muli pabwalo. 12Ndipo akakhala munthu waumphawi musagone
muli naco cikole cace; 13polowa dzuwa mumbwezeretu cikoleco,
kuti agone m'cobvala cace, ndi kukudalitsani; ndipo
kudzakukhalirani cilungamo pamaso pa Yehova Mulungu wanu.

Za cifundo pa anchito aumphawi, alendo ndi amasiye

14Musamasautsa wolembedwa nchito, wakukhala waumphawi ndi
wosauka, wa abale anu kapena wa alendo ali m'dziko mwanu,
m'midzi mwanu. 15Pa tsiku lace muzimpatsa kulipira kwace,
lisalowepo dzuwa; pakuti ndiye waumphawi, ndi mtima wace
ukhumba uku; kuti angakulirireni kwa Yehova, ndipo kukukhaireni
cimo.

16Atate asaphedwere ana, ndi ana asaphedwere atate; munthu
yense aphedwere cimo lace lace.
17Musamaipsa mlandu wa mlendo, kapena wa ana amasiye;
kapena kutenga cikole cobvala ca mkazi wamasiye; 18koma
muzikumbukila kuti munali akapolo m'Aigupto, ndi kuti Yehova
Mulungu wanu anakuombolaniko; cifukwa cace ndikuuzani kucita
cinthu ici.
19Mutasenga dzinthuzanu m'munda mwanu, ndipo mwaiwala
mtolo m'mundamo, musabwererako kuutenga; ukhale wa mlendo,
wa mwana wamasiye, ndi wa mkazi wamasiye; kuti Yehova
Mulungu wanu akudalitseni m'nchito zonse za manja anu.
20Mutagwedeza mtengo wanu wa azitona musayesenso nthambi
mutatha nazo; akhale a mlendo, a mwana wamasiye, ndi a mkazi
wamasiye. 21Mutachera m'munda wanu wamphesa, musakunkha
pambuyo panu; zikhale za mlendo, za mwana wamasiye, ndi za
mkazi wamasiye. 22Ndipo muzikumbukila kuti munali: akapolo
m'dziko la Aigupto; cifukwa cace ndikuuzani kucita cinthu ici.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Za makwapulidwe a wolakwa

1Pakakhala ndeu pakati pa anthu, nakapita kukaweruzidwa iwowa,
nakaweruza mlandu wao oweruza; azimasula wolungama,
namange woipa. 2Ndipo kudzali, wocita coipa akayenera
amkwapule, woweruza amgonetse kuti amkwapule pamaso pace,
amwerengere zofikira coipa cace. 3Amkwapule kufikira makumi
anai, asaonjezepo; pakuti, akaonjezapo ndi kumkwapula
mikwapulo yambiri, angapeputse mbale wanu pamaso panu.
4Musamapunamiza ng'ombe popuntha tirigu.

Za kukwatibwa mkazi ndi mlamu wace

5Abale akakhala pamodzi, nafa wina wa iwowa, wopanda mwana
wamwamuna, mkazi wa wafayo asakwatibwe ndi mlendo wakunja;
mbale wa mwamuna wace alowane naye, namtenge akhale mkazi
wace, namcitire zoyenera mbale wa mwamuna wace. 6Ndipo
kudzali, kuti woyamba kubadwa amene adzambala, adzalowa
dzina lace la mbale wace wafayo, kuti dzina lace lisafafanizidwe
m'Israyeli. 7Ndipo ngati mwamunayo safuna kutenga mkazi wa
mbale wace, mkazi wa mbale waceyo azikwera kumka kucipata,
kwa akuru, ndi kuti, Mbale wa mwamuna wanga akana kuutsira
mbale wace dzina m'Israyeli; safuna kundicitira ine zoyenera
mbale wa mwamuna. 8Pamenepo akuru a mudzi wace amuitane,
ndi kulankhula naye; ndipo akaimirira ndi kuti, Sindifuna
kumtenga; 9pamenepo mkazi wa mbale wace azimyandikiza
pamaso pa akuru, nacotse nsapato yace ku ph zi la mwamunayo,
ndi kumthira malobvu pankhope pace, ndi kumyankha ndi kuti,
Atere naye mwamuna wosamanga nyumba ya mbale
wace. 10Ndipo azimucha dzina lace m'Israyeli, Nyumba ya uje
anamcotsa nsapato.
11Akalimbana wina ndi mnzace, nakayandikiza mkazi wa winayo
kulanditsa mwamuna wace m'dzanja la wompandayo, nakaturutsa
dzanja lace, ndi kumgwira kudzibvalo; 12pamenepo muzidula
dzanja lace; diso lanu lisamcitire cifundo.
13Musamakhala nayo m'thumba mwanu miyala ya miyeso iwiri,
waukuru ndi waung'ono. 14Musamakhala nayo m'nyumba yanu
miyeso ya efa yosiyana, waukuru ndi waung'ono. 15Muzikhala nao
mwala wa muyeso wofikira ndi woyenera; mukhale nao muyeso wa
efa wofikira ndi woyenera; kuti masiku anu acuruke m'dziko limene
Yehova Mulungu wanu akupatsani. 16Pakuti onse akucita zinthu izi,
onse akucita cisalungamo, Yehova Mulungu wanu anyansidwa nao.

Amaleki afafanizike

17Kumbukilani cocitira inu Amaleki panjira, poturuka inu
m'Aigupto; 18kuti anakomana ndi inu panjira, nakantha onse ofok a
akutsala m'mbuyo mwanu, pakulema ndi kutopa inu; ndipo

sanaopa Mulungu, 19Ndipo kudzali, pamene Yehova Mulungu wanu atakupumulitsirani adani anu onse ozungulira, m'dziko limene Yehova Mulungu wanu akupatsani likhale colowa canu canu, kuti muzifafaniza cikumbutso ca Amaleki pansi pa thambo; musamaiwala.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Copereka ca zipatso zoyamba

1Ndipo kudzali, utakalowa m'dziko limene Yehova Mulungu wanu
akupatsani likhale colowa canu, ndipo mwacilandira ndi kukhala
m'mwemo; 2kuti muzitengako zoyamba za zipatso zonse za
nthaka, zakubwera nazo inu zocokera m'dziko limene Yehova
Mulungu wanu akupatsani; ndi kuziika mumtanga, ndi kupita ku
malo amene Yehova Mulungu wanu adzasankha kukhalitsako dzina
lace. 3Ndipo mufike kwa wansembe wakukhala m'masiku awa, ndi
kunena naye, Ndibvomereza lero lino kwa Yehova Mulungu wako,
kuti ndalowa m'dziko limene Yehova analumbirira makolo athu, kuti
adzatipatsa ili. 4Ndipo wansembe alandire mtanga m'manja
mwanu, ndi kuuika pa guwa la nsembe la Yehova Mulungu
wanu. 5Ndipo muyankhe ndi kuti pamaso pa Yehova Mulungu
wanu, Kholo langa ndiye M-aramu wakuti atayike, natsika kumka
ku Aigupto, nagoneragonera komweko ali nao anthu pang'ono,
nasandukako mtundu waukuru, wamphamvu, ndi wocuruka anthu
ace; 6koma Aaigupto anaticitira coipa, natizunza, natisenza nchito
yolimba. 7Pamenepo tinapfuulira kwa Yehova, Mulungu wa makolo
athu; ndipo Yehova anamva mau athu, napenya kuzunzika kwathu,
ndi nchito yathu yolemetsa, ndi kupsinjika kwathu; 8ndipo Yehova
anatiturutsa m'Aigupto ndi dzanja lamphamvu, ndi mkono
wotambasuka, ndi kuopsa kwakukuru, ndi zizindikilo, ndi
zodabwiza; 9ndipo anabwera nafe kumalo kuno, natipatsa dziko ili
ndilo dziko moyenda mkaka ndi uci ngati madzi. 10Ndipo tsopano,
taonani, ndabwera nazo zoyamba za zipatso za nthaka, zimene
Inu, Yehova, mwandipatsa. Ndipo muziike pamaso pa Yehova
Mulungu wanu, ndi kugwadira Yehova Mulungu wanu; 11ndipo
mukondwere nazo zokoma zonse zimene Yehova Mulungu wanu
akupatsani, inu ndi nyumba zanu, inu ndi Mlevi, ndi mlendo ali
pakati panu.

Limodzi la magawo khumi caka cacitatu

12Mutatha kugawa magawo khumi, zobala zanu zonse caka
cacitatu, ndico caka cogawa magawo khumi, muzizipereka kwa
Mlevi, kwa mlendo, kwa mwana wamasiye, ndi kwa mkazi
wamasiye, kuti adye m'midzi mwanu, ndi kukhuta. 13Ndipo
munene pamaso pa Yehova Mulungu wanu, Ndacotsa zopatulika
m'nyumba mwanga, ndi kuzipereka kwa Mlevi, ndi kwa mlendo, ndi
kwa mwana wamasiye, ndi kwa mkazi wamasiye, monga mwa
lamulo lanu lonse munandilamulira ine; sindinalakwira malamulo
anu, kapena kuwaiwala. 14Sindinadyako m'cisoni canga, kapena
kucotsako podetsedwa, kapena kuperekako kwa akufa; ndamvera
mau a Yehova Mulungu wanga; ndacita monga mwa zonse
munandilamulira ine. 15Penyani muli mokhalamo mwanu

mopatulika, m'mwamba, ndipo dalitseni anthu anu Israyeli, ndi nthaka imene munatipatsa, monga munalumbirira makolo athu, dziko moyenda mkaka ndi uci ngati madzi.
16Lero lino Yehova Mulungu wanu akulamulirani kucita malemba ndi maweruzo awa; potero muzimvera ndi kuwacita ndi mtima wanu wonse, ndi moyo wanu wonse. 17Mwalonjezetsa Yehova lero kuti adzakhala Mulungu wanu, ndi kuti mudzayenda m'njira zace, ndi kusunga malemba ace, ndi malamulo ace, ndi maweruzo ace, ndi kumvera mau ace. 18Ndipo Yehova wakulonjezetsani lero kuti mudzakhala anthu ace ace a pa okha, monga ananena ndi inu, ndi kuti mudzasunga malamulo ace onse; 19kuti akukulitseni koposa amitundu onse anawalenga, wolemekezeka, womveka dzina, ndi waulemu; ndi kuti mukhale mtundu wa anthu wopatulikira Yehova Mulungu wanu monga ananena.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Za kuutsa miyala va cikumbutso ataoloka Yordano

1Ndipo Mose ndi akuru a Israyeli anauza anthu, nati, Sungani
malamulo onse ndikuuzani lero. 2Ndipo kudzali, tsiku lakuoloka inu
Yordano kulowa dziko limene Yehova Mulungu wanu akupatsani,
kuti mudziutsire miyala yaikuru, ndi kuimata ndi njeresa; 3ndipo
mulemberepo mau onse a cilamulo ici, mutaoloka; kuti mulowe
m'dziko limene Yehova Mulungu wanu akupatsani, dziko moyenda
mkaka ndi uci ngati madzi, monga Yehova Mulungu wa makolo anu
ananena ndi inu. 4Ndipo kudzali, mutaoloka Yordano, muutse
miyala iyi ndikuuzani lero, m'phiri la Ebala, ndi kuimata ndi
njeresa. 5Ndipo komweko mumangire Yehova Mulungu wanu guwa
la nsembe, guwa la nsembe lamiyala; musakwezepo cipangizo
cacitsulo. 6Mumange guwa la nsembe la Yehova Mulungu wanu
lamiyala yosasema; ndi kuperekapo nsembe zopsereza kwa Yehova
Mulungu wanu; 7ndi kuphera nsembe zoyamika, ndi kudyapo, ndi
kukondwera pamaso pa Yehova Mulungu wanu. 8Ndipo mulembere
pa miyalayi mau onse a cilamulo ici mopenyeka bwino.
9Ndipo Mose, ndi ansembe Alevi ananena ndi Israyeli wonse, ndi
kuti, Khalani cete, imvanitu, Israyeli; lero lino mwasanduka mtundu
wa anthu wa Yehova Mulungu wanu. 10Potero muzimvera mau a
Yehova Mulungu wanu, ndi kucita malamulo ace, ndi malemba ace,
amene ndikuuzani lero lino.

Mdalitso ndi temberero ku Gerizimu ndi Ebola

11Ndipo Mose anauza anthu tsiku lomwelo, ndi kuti, 12Aimirire awa
pa phiri la Gerizimu kudalitsa anthu, mutaoloka Yordano: Simeoni
ndi Levi, ndi Yuda, ndi Isakara, ndi Yosefe, ndi
Benjamini. 13Naimirire awa pa phiri la Ebala, kutemberera: Rubeni,
Gadi, ndi Aseri, ndi Zebuloni, Dani, ndi Nafitali. 14Ndipo ayankhe
Alevi ndi kunena kwa amuna onse a Israyeli, ndi mau omveka.
15Wotembereredwa munthu wakupanga fano losema kapena
loyenga, lonyansidwa nalo Yehova, nchito ya manja a mmisiri, ndi
kuliika m'malo a m'tseri. Ndipo anthu onse: ayankhe ndi kuti,
Amen.
16Wotembereredwa iye wakupeputsa atate wace kapena mai wace.
Ndi anthu onse anene, Amen.
17Wotembereredwa iye wakusendeza malire a mnansi wace. Ndi
anthu onse anene, Amen.
18Wotembereredwa wakusokeretsa wakhungu m'njira, Ndi anthu
onse anene, Amen.
19Wotembereredwa iye wakuipsa mlandu wa mlendo, mwana
wamasiye, ndi mkazi wamasiye. Ndi anthu onse anene, Amen.
20Wotembereredwa iye wakugona ndi mkazi wa atate wace;
popeza wabvula atate wace. Ndi anthu onse anene, Amen.

21Wotembereredwa iye wakugona ndi nyama iri yonse. Ndi anthu onse anene, Amen.
22Wotembereredwa iye wakugona ndi mlongo wace, mwana wamkazi wa atate wace, kapena mwana wamkazi wa mace. Ndi anthu onae anene, Amen.
23Wotembereredwa iye wakugona ndi mpongozi wace. Ndi anthu onse anene, Amen.
24Wotembereredwa iye wakukantha mnansi wace m'tseri. Ndi anthu onse anene, Amen.
25Wotembereredwa iye wakulandira camwazi cakuti akanthe munthu wosacimwa. Ndi anthu onse anene, Amen.
26Wotembereredwa iye wosabvomereza mau a cilamulo ici kuwacita. Ndi anthu onse anene, Amen.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Madalitso pa kumvera kwao

1Ndipo kudzali, mukadzamvera mau a Yehova Mulungu wanu
mwacangu, ndi kusamalira kucita malamulo ace onse amene
ndikuuzani lero, kuti Yehova Mulungu wanu adzakukulitsani koposa
amitundu onse a pa dziko lapansi; 2ndipo madalitso awa onse
adzakugwerani, ndi kukupezani, mukadzamvera mau a Yehova
Mulungu wanu. 3Mudzakhala odala m'mudzi, ndi odala
kubwalo. 4Zidzakhala zodala zipatso za thupi lanu, ndi zipatso za
nthaka yanu, ndi zipatso za zoweta zanu, zoswana za ng'ombe
zanu, ndi zoswana za nkhosa zanu. 5Zidzakhala zodala mtanga
wanu, ndi coumbiramo mkate wanu. 6Mudzakhala odala polowa
inu, mudzakhala odala poturuka inu. 7Yehova adzakantha adani
anu akukuukirani; adzakudzerani njira imodzi, koma adzathawa
pamaso panu njira zisanu ndi ziwiri. 8Yehova adzakulamulirani
dalitso m'nkhokwe zanu, ndi m'zonse muturutsirako dzanja lanu;
ndipo adzakudalitsani m'dziko limene Yehova Mulungu wanu
akupatsani, 9Yehova adzakukhazikirani yekha mtundu wa anthu
wopatulika, monga anakulumbirirani; ngati mudzasunga malamulo
a Yehova Mulungu wanu, ndi kuyenda m'njira zace. 10Ndipo anthu
onse a pa dziko lapansi adzaona kuti akuchulani dzina la Yehova;
nadzakuopani. 11Ndipo Yehova adzakucurukitsirani zokoma,
m'zipatso za thupi lanu, ndi m'zipatso za zoweta zanu, ndi
m'zipatso za nthaka yanu, m'dziko limene Yehova analumbirira
makolo anu kuti adzakupatsani ilo, 12Yehova adzakutsegulirani
cuma cace cokoma, ndico thambo la kumwamba, kupatsa dziko
lanu mvula m'nyengo yace, ndi kudalitsa nchito zonae za dzanja
lanu; ndipo mudza kongoletsa amitundu ambiri, osakongola
nokha. 13Ndipo Yehova adzakuyesani mutu, si mcira ai; ndipo
mudzakhala wa pamwamba pokha, si wapansi ai; ngati
mudzamvera malamulo a Yehova Mulungu wanu, amene
ndikuuzani lero, kuwasunga ndi kuwacita; 14osapatukira mau ali
onse ndikuuzani lero, kulamanja, kapena kulamanzere, kutsata
milungu yina kuitumikira.

Matemberero pa kusamvera kwao

15Koma kudzali, mukapanda kumvera mau a Yehova Mulungu
wanu, kusamalira kucita malamulo ace onse ndi malemba ace
amene ndikuuzani lero, kuti matemberero awa onse
adzakugwerani ndi kukupezani, 16Mudzakhala otembereredwa
m'mudzi, ndi otembereredwa pabwalo. 17Zidzakhala
zotembereredwa mtanga wanu ndi coumbiramo mkate
wanu. 18Zidzakhala zotembereredwa zipatso za thupi lanu, ndi
zipatso za nthaka yanu, zoswana za ng'ombe zanu, ndi zoswana za
nkhosa zanu. 19Mudzakhala otembereredwa polowa inu, ndi

otembereredwa poturuka inu. 20Yehova adzakutumizirani
temberero, cisokonezeko, ndi kudzudzula monsemo mukaturutsa
dzanja lanu kucita kanthu, kufikira mwaonongeka, kufikira
mwatayika rosanga, cifukwa ca zocita inu zoipa, zimene wandisiya
nazo, 21Yehova adzakumamatiritsani mliri kufikira akakuthani
kukucotsani kudziko, kumene mupitako kulilandira. 22Yehova
adzakukanthani ndi nthenda yoondetsa ya cifuwa, ndi malungo,
ndi cibayo, ndi kutentha thupi, ndi lupanga, cinsikwi ndi cinoni;
ndipo zidzakutsatani kufikira mwatayika. 23Ndipo thambo lanu la
pamwamba pamutu panu lidzakhala ngati mkuwa, ndi dziko liri
pansi panu ngati citsulo. 24Yehova adzasanduliza mvula ya dziko
lanu ikhale pfumbi ndi phulusa; zidzakutsikirani kucokera
kumwamba, kufikira mwaonongeka. 25Yehova adzalola adani anu
akukantheni; mudzawaturukira njira imodzi, koma mudzawathawa
pamaso pao njira zisanu ndi ziwiri, ndipo mudzagwedezeka pakati
pa maufumu onse a dziko lapansi. 26Ndipo mitembo yanu
idzakhalacakudya ca mbalame zonse za m'mlengalenga, ndi
zirombo zonse za pa dziko lapansi, ndipo palibe
wakuziingitsa. 27Yehova adzakukanthani ndi zirombo za ku Aigupto,
ndi nthenda yoturuka mudzi, ndi cipere, ndi mphere, osacira
nazo. 28Yehova adzakukanthani ndi misala, ndi khungu, ndi
kuzizwa mumtima; 29ndipo mudzafufuza usana, monga wakhungu
amafufuza mumdima, ndipo simudzapindula nazo njira zanu; koma
mudzakhala wopsinjika, nadzakuberani masiku onse, wopanda
wina wakukupulumutsani. 30Mudzaparana ubwenzi ndi mkazi,
koma mwamuna wina adzagona naye; mudzamanga nyumba,
osakhala m'mwemo; mudzanka munda wamphesa, osalawa
zipatso zace. 31Adzapha ng'ombe yanu pamaso panu, osadyako
inu; adzalanda buru wanu molimbana pamaso panu,
osakubwezerani; adzapereka nkhosa zanu kwa adani anu,
wopanda wina wakukupulumutsani. 32Adzapereka ana anu amuna
ndi akazi kwa anthu a mtundu wina, ndipo m'maso mwanu
mudzada ndi kupenyerera, powalirira tsiku lonse; koma mulibe
mphamvu m'dzanja lanu. 33Mtundu wa anthu umene simudziwa
udzadya zipatso za nthaka yanu ndi nchito zanu zonse; ndipo
mudzakhala wopsinjika ndi wophwanyika masiku
onse; 34nimudzakhala oyeruka cifukwa comwe muciona ndi maso
anu, 35Yehova adzakukanthani ndi cironda coipa cosacira naco
kumaondo, ndi kumiyendo, kuyambira pansi pa phazi lanu kufikira
pamwamba pa mutu panu. 36Yehova adzamukitsa inu, ndi mfumu
yanu imene mudzadziikira, kwa mtundu wa anthu umene
simudziwa, inu kapena makolo anu; ndipo mudzatumikirako
milungu yina ya mitengo ndi miyala. 37Ndipo mudzakhala
codabwitsa, ndi nkhani, ndi nthanthi, mwa mitundu yonse ya anthu

amene Yehova akutsogoleraniko. 38Mudzaturuka nazo mbeu zambiri kumunda, koma mudzakolola pang'ono; popeza dzombe lidzazitha. 39Mudzanka m'minda yamphesa ndi kuilima, koma osamwa vinyo wace, kapena kuchera mphesa zace, popeza citsenda cidzaidya. 40Mudzakhala nayo mitengo yaazitona m'malire anu onset osadzola mafuta; popeza zipatso za mitengo yaazitona zidzapululuka. 41Mudzabala ana amuna ndi akazi, osakhala nao, popeza adzalowa ukapolo. 42Mitengo yanu yonse ndi zipatso za nthaka yanu zidzakhala zao zao za dzombe. 43Mlendo wokhala pakati panu adzakulira-kulira inu, koma inu mudzacepera-cepera. 44Iye adzakukongoletsani, osamkongoletsa ndinu; iye adzakhala mutu, koma inu ndinu mcira. 45Ndipo matemberero awa onse adzakugwerani, nadzakulondolani, ndi kukupezani, kufikira mwaonongeka, popeza simunamvera mau a Yehova Mulungu wanu, kusunga malamulo ace ndi malemba ace amene anakulamulirani; 46ndipo zidzakukhalirani inu ndi mbeu zanu ngati cizindikilo ndi cozizwa, nthawi zonse. 47Popeza simunatumikira Yehova Mulungu wanu ndi cimwemwe ndi mokondwera mtima, cifukwa ca kucuruka zinthu zonse; 48cifukwa cace mudzatumikira adani anu amene Yehova adzakutumizirani, ndi njala, ndi ludzu, ndi usiwa, ndi kusowa zinthu zonse; ndipo adzaika goli lacitsulo pakhosi panu, kufikira atakuonongani. 49Yehova adzakutengerani mtundu wa anthu wocokera kutali ku malekezero a dziko lapansi, monga iuluka mphungu; mtundu wa anthu amene simunamva malankhulidwe ao; 50mtundu wa anthu wa nkhope yaukali, wosamalira nkhope ya wokalamba, wosamcitira cifundo mwana; 51ndipo adzadya zipatso za ng'ombe zanu, ndi zipatso za nthaka yanu, kufikira mwaonongeka; osakusiyirani tirigu, vinyo, kapena mafuta, zoswana ng'ombe zanu, zoswana nkhosa zanu, kufikira atakuonongani. 52Ndipo adzakuzingani m'midzi mwanu monse, kufikira adagwa malinga anu atali ndi olimba, amene munawakhulupirira, m'dziko lanu lonse; inde, adzakuzingani m'midzi mwanu monse, m'dziko lanu lonse limene Yehova Mulungu wanu akupatsani. 53Ndipo mudzadya cipatso ca thupi lanu, nyama ya ana anu amuna ndi akazi amene Yehova Mulungu wanu anakupatsani; pakukumangirani tsasa ndi kukupsinjani adani anu. 54Mwamuna wololopoka nkhongono ndi wanyonga pakati pa inu diso lace lidzaipira mbale wace, ndi mkazi wa pa mtima wace, ndi ana ace otsalira; 55osapatsako mmodzi yense wa iwowa nyama ya ana ace alinkudyayo, popeza sikamtsalira kanthu; pakukumangirani tsasa ndi kukupsinjani mdani wanu m'midzi mwanu monse. 56Mkazi wololopoka nkhongono ndi wanyonga pakati pa inu, wosayesa kuponda pansi ndi phazi lace popeza ndiye wanyonga, ndi wololopoka nkhongono, diso lace lidzamuipira

mwamuna wa pamtima pace, ndi mwana wace wamwamuna ndi wamkazi; 57ndico dfukwa ca matenda akuturuka pakati pa mapazi ace, ndi ana ace adzawabala; popeza adzawadya m'tseri posowa zinthu zonse; pakukumangirani tsasa ndi kukupsinjani mdaniwanu m'midzi mwanu. 58Mukapanda kusamalira kucita mau onse a cilamulo ici olembedwa m'buku ili, kuopa dzina ili la ulemerero ndi loopsa, ndilo YEHOVA MULUNGU ANU; 59Yehova adzacita miliri yanu ndi ya ana anu ikhale yodabwiza, miliri yaikuru ndi yokhalitsa, ndi nthenda zoipa ndi zokhalitsa. 60Ndipo adzakubwezerani nthenda zonse za Aigupto, zimene munaziopa; ndipo zidzakumamatirani inu. 61Ndiponso nthenda zonse ndi miliri yonse zosalembedwa m'buku la cilamulo ici, Yehova adzakutengerani izi, kufikira mwaonongeka. 62Ndipo mudzatsala anthu pang'ono, mungakhale mukacuruka ngati nyenyezi za m'mwamba; popeza simunamvera mau a Yehova Mulungu wanu. 63Ndipo kudzali kuti, monga Yehova anakondwera nanu kukucitirani zabwino, ndi kukucurukitsani; momwemo Yehova adzakondwera nanu kutayikitsa ndi kuononga inu, ndipo adzakuzulani kudziko kumene mulowako kulilandira. 64Ndipo Yehova adzakubalalitsani mwa mitundu yonse ya anthu, kuyambira malekezero a dziko lapansi kufikira malekezero a dziko lapansi; ndipo kumeneko mudzatumikira milungu yina, imene simunaidziwa, inu ndi makolo anu, yamitengo ndi yamiyala. 65Ndipo mwa a mitundu iyi simudzapumula, inde sipadzakhala popumulira phazi lanu; koma Yehova adzakupatsani kumeneko mtima wonjenjemera, m'maso mwanu mudzada, mudzafa ndi kulefuka mtima. 66Ndipo moyo wanu udzakhala wanjiranjira pamaso panu, ndipo mudzacita mantha usiku ndi usana, osakhazika mtima za moyo wanu. 67M'mawa mudzati, Mwenzi atafika madzulo! ndi madzulo mudzati, Mwenzi utafika m'mawa! cifukwa ca mantha a m'mtima mwanu amene mudzaopa nao, ndi cifukwa ca zopenya maso anu zimene mudzazipenya. 68Ndipo Yehova adzakubwezerani ku Aigupto ndi ngalawa, pa njira imene ndinati kwa inu, kuti, Simudzaionanso; ndipo kumeneko mudzadzigulitsa kwa adani anu mukhale akapolo ndi adzakazi; koma palibe wogulainu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Mulungu abwereza kupangana nao

1Awa ndi mau a cipangano cimene Yehova analamulira Mose
acicite ndi ana a Israyeli m'dziko la Moabu, pamodzi ndi
cipanganoco anacita nao m'Horebe.
2Ndipo Mose anaitana Israyeli wonse, nati nao, Munapenya inu
zonse zimene Yehova anacitira Farao, ndi anyamata ace onse, ndi
dziko lace lonse, pamaso panu m'dziko la Aigupto; 3mayesero
akuruwa maso anu anawapenya, zizindikilozo, ndi zozizwa zazikuru
zija; 4koma Yehova sanakupatsani mtima wakudziwa, ndi maso
akupenya, ndi makutu akumva, kufikira lero lino. 5Ndipo
ndinakutsogolerani zaka makumi anai m'cipululu; zobvala zanu
sizinatha pathupi panu, ndi nsapato zanu sizinatha pa phazi
lanu. 6Simunadya mkate, simunamwa vinyo kapena cakumwa
colimba; kuti mudziwe kuti Ine ndine Yehova Mulungu
wanu. 7Ndipo pamene munafika pamalo pano, Sihoni mfumu ya
Hesiboni, ndi Ogi mfumu ya Basana, anaturuka kudzakomana nafe
kunkhondo, ndipo tinawakantha; 8ndipo tinalanda dziko lao, ndi
kulipereka likhale colowa cao ca Arubeni, ndi Agadi, ndi pfuko la
hafu la Manase. 9Cifukwa cace sungani mau a cipangano ici ndi
kuwacita, kuti mucite mwanzeru m'zonse muzicita.
10Muimirira inu nonse lero lino pamaso pa Yehova Mulungu wanu;
mafumu anu, mapfuko anu, akuru anu, ndi akapitao anu, amuna
onse a Israyeli; 11makanda anu, akazi anu, ndi mlendo wanu
wakukhala pakati pa zigono zanu, kuyambira wotema nkhuni
kufikira wotunga madzi; 12kuti mulowe cipangano ca Yehova
Mulungu wanu, ndi lumbiriro lace, limene Yehova Mulungu wanu
acita ndi inu lero lino; 13kuti adzikhazikire inu, mtundu wace wa
anthu lero lino, ndi kuti akhale kwa inu Mulungu, monga ananena
ndi inu, ndi monga analumbirira makolo anu, Abrahamu, Isake, ndi
Yakobo. 14Koma sindicita cipangano ici ndi lumbiro ili ndi inu
nokha; 15komanso ndi iye wakuimirira pano nafe lero lino pamaso
pa Yehova Mulungu wathu, ndiponso ndi iye wosakhala pano nafe
lero lino. 16Pakuti mudziwa cikhalidwe cathu m'dziko la Aigupto, ndi
kuti tinapyola pakati pa amitundu amene munawapyola; 17ndipo
munapenya zonyansa zao, ndi mafano ao, mtengo ndi mwala,
siliva ndi golidi, zokhala pakati pao; 18kuti angakhale pakati pa inu
mwamuna, kapena mkazi, kapena banja, kapena pfuko, mtima wao
watembenuka kusiyana naye Yehova Mulungu wathu lero lino, kuti
apite ndi kutumikira milungu ya amitundu aja; kuti ungakhale
pakati pa inu muzu wakubala ndulu ndi cowawa. 19Ndipo
kungakhale, akamva mau a lumbiro ili adzadzidalitsa m'mtima
mwace, ndi kuti, Ndidzakhala nao mtendere, ndingakhale ndiyenda
nao mtima wanga wopulukira, kuledzera nditamva ludzu; 20Yehova

sadzamkhululukira, koma pamenepo mkwiyo wa Yehova ndi nsanje
yace zidzamfukira munthuyo; ndipo temberero lonse lolembedwa
m'buku ili lidzamkhalira; ndipo Yehova adzafafaniza dzina lace
pansi pa thambo. 21Ndipo Yehova adzamsiyanitsa ndi mafuko onse
a Israyeli ndi kumcitira coipa, monga mwa matemberero onse a
cipangano colembedwa m'buku ili la cilamulo. 22Ndipo mbadwo
ukudza, ana anu akuuka mutafa inu, ndi mlendo wocokera ku dziko
lakutali, adzati, pakuona iwo miliri ya dziko ili, ndi nthendazi;
Yehova awadwalitsa nazo, 23ndi kuti lidapsa dziko lace lonse ndi
sulfure, ndi mcere, kuti sabzalamo, kapena siliphukitsa kanthu
kapena sumerapo msipu, monga kupasula kwace kwa Sodomu ndi
Gomora, Adima, ndi Zeboimu, imene Yehova anaipasula m'mkwiyo
wace ndi ukali wace; 24inde amitundu onse adzati, Yehova
anacitira dziko ili cotero cifukwa ninji? nciani kupsa mtima
kwakukuru kumene? 25Pamenepo adzati, Popeza analeka
cipangano ca Yehova, Mulungu wa makolo ao, cimene anacita nao
pakuwaturutsa m'dziko la Aigupto; 26napita natumikira milungu
yina, naigwadira, milungu imene sanaidziwa, imene
sanawagawira; 27cifukwa cace Mulungu anapsera mtima dziko ili
kulitengera temberero lonse lolembedwa m'buku ili. 28Ndipo
Yehova anawazula m'nthaka mwao mokwiya ndi mozaza, ndi
m'ukali waukuru, nawaponya m'dziko lina, monga lero
lino. 29Zinsinsi nza Yehova Mulungu wathu; koma zobvumbuluka
nza ife ndi ana athu kosatha, kuti ticite mau onse a cilamulo ici.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Mulungu alonjeza kuwalanditsa akalapa atacimwa

1Ndipo kudzakhala, zikakugwerani zonsezi, mdalitso ndi temberero,
ndinaikazi pamaso panu, ndipo mukazikumbukila mumtima mwanu
mwa amitundu onse, amene Yehova Mulungu wanu
anakupitikitsiraniko; 2nimukabwerera kwa Yehova Mulungu wanu,
ndi kumvera mali ace, monga mwa zonse ndikuuzani lero lino, inu
ndi ana anu, ndi mtima wanu wonse, ndi moyo wanu
wonse; 3pamenepo Yehova Mulungu wanu adzaucotsa ukapolo
wanu, ndi kukucitirani cifundo; nadzabwera ndi kukumemezani
mwa mitundu yonse ya anthu, kumene Yehova Mulungu wanu
anakubalalitsiraniko. 4Otayika anu akakhala ku malekezero a
thambo, Yehova Mulungu wanu adzakumemezani kumeneko,
nadzakutenganiko; 5ndipo Yehova Mulungu wanu adzakulowetsani
m'dziko lidakhala lao lao la makolo anu, nilidzakhala lanu lanu;
ndipo adzakucitirani zokoma, ndi kukucurukitsani koposa makolo
anu. 6Ndipo Yehova Mulungu wanu adzakudulani mtima wanu ndi
mtima wa mbeu zanu, kuti mukonde Yehova Mulungu wanu ndi
mtima wanu wonse, ndi moyo wanu wonse, kuti mukhale ndi
moyo. 7Ndipo Yehova Mulungu wanu adzaika matemberero awa
onse pa adani anu, ndi iwo akukwiya ndi inu, amene
anakulondolani. 8Pamenepo mutembenuke ndi kumvera mau a
Yehova, ndi kucita malamulo ace onse amene ndikuuzani lero
lino. 9Ndipo Yehova Mulungu wanu adzakucurukitsirani nchito
zonse za dzanja lanu, zipatso za thupi lanu, ndi zipatso za zoweta
zanu, ndi zipatso za nthaka yanu, zikukomereni; popeza Yehova
Mulungu wanu adzakondweranso kukucitirani zokoma; monga
anakondwera ndi makolo anu; 10ngati mudzamvera mau a Yehova
Mulungu wanu, kuwasunga malamulo ace ndi malemba ace
olembedwa m'buku la cilamulo ici; ngati mudzabwerera kudza kwa
Yehova Mulungu wanu ndi mtima wanu wonse, ndi moyo wanu
wonse.
11Pakuti lamulo ili ndikuuzani lero lino, silikulakani kulizindikira,
kapena silikhala kutali. 12Silikhala m'mwamba, kuti mukati,
Adzatikwerera m'mwamba ndani, ndi kubwera nalo kwa ife, ndi
kutimvetsa ili, kuti tilicite? 13Ndipo silikhala tsidya la nyanja, kuti
mukati, Adzatiolokera ndani tsidya la nyanja, ndi kutitengera ili, ndi
kutimvetsa ili, kuti tilicite? 14Pakuti mauwa ali pafupifupi ndi inu,
m'kamwa mwanu, ndi m'mtima mwanu, kuwacita.
15Tapenyani, ndaika pamaso panu lero lino moyo ndi zokoma, imfa
ndi zoipa; 16popeza ndikuuzani lero kukonda Yehova Mulungu
wanu, kuyenda m'njira zace, ndi kusunga malamulo ace ndi
malemba ace ndi maweruzo ace, kuti mukakhale ndi moyo ndi
kucuruka, ndi kuti Yehova Mulungu wanu akakudalitseni m'dziko

limene mulowako kulilandira. 17Koma mukatembenukira mtima
wanu, osamvera inu, nimukaceteka, ndi kugwadira milungu yina
ndi kuitumikira; 18ndikulalikirani inu lero, kuti mudzatayika ndithu,
masiku anu sadzacuruka m'dziko limene muolokera Yordano
kulowamo kulilandira. 19Ndicititsa mboni lero kumwamba ndi dziko
lapansi zitsutse inu; ndaika pamaso panu moyo ndi imfa, mdalitso
ndi temberero; potero, sankhani moyo, kuti mukhale ndi moyo, inu
ndi mbeu zanu; 20kukonda Yehova Mulungu wanu, kumvera mau
ace, ndi kummamatira iye, tr pakuti iye ndiye moyo wanu, ndi
masiku anu ocuruka; kuti mukhale m'dziko limene Yehova
analumbirira makolo anu, Abrahamu, Isake, ndi Yakobo, kuwapatsa
ili.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Yoswa adzalowa m'malo a Mose

1Ndipo Mose anamuka nanena mau awa kwa Israyeli wonse, 2nati
nao, Ndine munthu wa zaka zana ndi makumi awiri lero lino;
sindikhozanso kuturuka ndi kulowa ndipo Yehova anati kwa ine,
Sudzaoloka Yordano uyu. 3Yehova Mulungu wanu ndiye adzaoloka
pamaso panu, iye ndiye adzaononga amitundu awo pamaso panu,
ndipo mudzawalandira. Yoswa ndiye adzakutsogolerani pooloka,
monga ananena Yehova. 4Ndipo Yehova adzawacitira monga
anacitira Sihoni ndi Ogi, mafumu a Aamori, ndi dziko lao limene
analiononga. 5Yehova akadzawapereka pamaso panu, muziwacitira
monga mwa lamulo lonse ndakuuzani. 6Khalani amphamvu,
limbikani mitima, musamacita mantha, kapena kuopsedwa cifukwa
ca iwowa; popeza Yehova Mulungu wanu ndiye amene amuka
nanu; iye sadzakusowani, kapena irukusiyani. 7Ndipo Mose
anaitana Yoswa, nati naye pamaso pa Israyeli wonse, Khala
wamphamvu, nulimbe mtima; pakuti udzalowa nao anthu awa
m'dziko limene Yehova analumbirira makolo ao kuwapatsa ilo;
ndipo iwe udzawalandiritsa ilo. 8Ndipo Yehova, iye ndiye amene
akutsogolera; iye adzakhala ndi iwe, iye sadzakusowa kapena
kukusiya; usamacita mantha, usamatenga nkhawa.

Pakutha zaka 7 ziri zonse azilalikira cilamuloco

9Ndipo Mose analembera cilamulo ici, nacipereka kwa ansembe,
ana a Levi, akunyamula likasa la cipangano la Yehova, ndi kwa
akuru onse a Israyeli, 10Ndipo Mose anawauza, ndi kuti, Pakutha
pace pa zaka zisanu ndi ziwiri, pa nyengo yoikika ya m'caka
cakulekerera, pa madyerero a misasa; 11pakufika Israyeli wonse
kuoneka pamaso pa Yehova Mulungu wanu, m'malo amene
adzasankha, muzilalikira cilamulo ici pamaso pa Israyeli wonse,
m'makutu mwao. 12Sonkhanitsan; anthu, amuna ndi akazi ndi ana
ang'ono, ndi mlendo wokhala m'midzi mwanu, kuti amve, ndi kuti
aphunzire kuopa Yehova Mulungu wanu, ndi kusamalira kucita mau
onse a cilamulo ici; 13ndi kuti ana ao osadziwa amve, oaphunzire
kuopa Yehova Mulungu wanu, masiku onse akukhala ndi moyo inu
kudziko kumene muolokera Yordano kulilandira likhale lanu lanu.

Yoswa asenza udindo wace

14Ndipo Yehova anati kwa Mose, Taona, ayandikira masiku ako
akuti uyenera kufa; kaitane Yoswa, nimuoneke m'cihema
cokomanako, kuti ndimlangize. Namuka Mose ndi Yoswa, naoneka
m'cihema cokomanako. 15Ndipo Yehova anaoneka m'cihema,
m'mtambo njo; ndipo mtambo njo unaima pa khomo la
cihema. 16Ndipo Yehova anati kwa Mose, Taona, udzagona tulo ndi
makolo ako; ndi anthu awa adzauka, oadzatsata ndi cigololo
milungu yacilendo ya dziko limene analowa pakati pace,

nadzanditava Ine, ndi kutyola cipangano canga ndinapangana naoco. 17Pamenepo ndidzawapsera mtima tsiku ilo, ndipo ndidzawataya, ndi kuwabisira nkhope yanga, ndipo adzathedwa, ndi zoipa ndi zobvuta zambiri zidzawafikira; kotero kuti adzati tsiku lija, Sizitifikira kodi zoipa izi popeza Mulungu wathu sakhala pakati pa ife? 18Koma Ine ndidzabisatu nkhope yanga tsiku lija cifukwa ca zoipa zonse adazicita; popeza anadzitembenukira milungu yina. 19Ndipo tsopano mudzilemberere nyimbo iyi, ndi kuphunzitsa ana a Israyeli iyi: mulike m'kamwa mwao, kuti nyimbo iyi indicitire mboni yotsutsa ana a Israyeli. 20Pakuti nditakalowetsa awa m'dziko limene ndinalumbirira makolo ao, moyenda mkaka ndi uci ngati madzi; ndipo atadya nakhuta, nanenepa, pamenepo adzatembenukira milungu yina, ndi kuitumikira, ndi kundipeputsa Ine, ndi kutyola cipangano canga. 21Ndipo kudzakhala, zitawafikira zoipa ndi zobvuta zambiri, nyimbo iyi idzacita mboni pamaso pao; popeza siidzaiwalika m'kamwa mwa mbeu zao; popeza ndidziwa zolingirira zao azicita lero lino, ndisanawalowetse m'dziko limene ndinalumbira. 22Potero Mose analembera nyimboyi tsiku lomweli, naiphunzitsa ana a Israyeli. 23Ndipo anauza Yoswa mwana wa Nuni, nati, Khala wamphamvu, nulimbe mtima; pakuti udzalowa nao ana a Israyeli m'dziko limene ndinawalumbirira: ndipo Ine ndidzakhala ndi iwe.
24Ndipo kunali, Mose atatha kulembera mau a cilamulo ici m'buku, kufikira atalembera onse, 25Mose anauza Alevi akunyamula likasa la cipangano la Yehova, ndi kuti, 26Landirani buku ili la cilamulo, nimuliike pambali pa likasa la cipangano la Yehova Mulungu wanu, likhale komweko mboni yakutsutsa inu. 27Pakuti ndidziwa kupikisana kwanu, ndi kupulukira kwanu; taonani, pokhala ndikali ndi moyo pamodzi ndi inu lero, mwapikisana ndi Yehova: koposa kotani nanga nditamwalira ine! 28Ndisonkhanitsire akuru onse a mapfuko anu, ndi akapitao anu, kuti ndinene mau awa m'makutu mwao, ndi kucititsa mboni kumwamba ndi dziko lapansi zitsutse iwo. 29Pakuti ndidziwa kuti nditamwalira ine mudzadziipsa ndithu, ndi kupatuka m'njira imene ndinakuuzani; ndipo cidzakugwerani coipa masiku otsiriza; popeza mudzacita coipa pamaso pa Yehova, kuutsa mkwiyo wace ndi nchito za manja anu.
30Ndipo Mose ananena mau a nyimbo iyi m'makutu mwa msonkhano wonse wa Israyeli, kufikira adatha.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Nyimbo adailemba Mose

1Kumwamba kuchere khutu, ndipo ndidzanena;
Ndi dziko lapansi limve mau a m'kamwa mwanga;
2Ciphunzitso canga cikhale ngati mvula;
Maneno anga agwe ngati mame;
Ngati mvula yowaza pamsipu,
Ndi monga madontho a mvula pazitsamba.
3Pakuti ndidzalalika dzina la Yehova;
Nenani kuti Mulungu wathu ndi wamkulu.
4Thanthwe, nchito yace ndi yangwiro;
Pakuti njira zace zonse ndi ciweruzo;
Mulungu wokhulupirika ndi wopanda cisalungamo;
Iye ndiye wolungama ndi wolunjika,
5Anamcitira zobvunda si ndiwo ana ace, cirema ncao;
Iwo ndiwo mbadwo wopulukira ndi wokhotakhota.
6Kodi mubwezera Yehova cotero,
Anthu inu opusa ndi opanda nzeru?
Kodi si ndiye Atate wanu, Mbuyewanu;
Anakulengani, nakukhazikitsani?
7Kumbukirani masiku akale,
Zindikirani zaka za mibadwo yambiri;
Funsani atate wanu, adzakufotokozerani;
Akuru anu, adzakuuzani.
8Pamene Wam'mwambamwamba anagawira amitundu colowacao,
Pamene anagawa ana a anthu,
Anaika malire a mitundu ya anthu,
Monga mwa kuwerenga kwao kwa ana a Israyeli,
9Pakuti gawo la Yehova ndilo anthu ace;
Yakobo ndiye muyeso wa colowacace.
10Anampeza m'dziko la mabwinja, ndi m'cipululu colira copanda kanthu;
Anamzinga, anamlangiza,
Anamsunga ngati kamwana lea m'diso;
11Monga mphungu ikasula cisa cace,
Nikapakapa pa ana ace,
Iye anayala mapiko ace, nawalandira,
Nawanyamula pa mapiko ace;
12Yehova yekha anamtsogolera,
Ndipo palibe mulungu wacilendo naye.
13Anamuyendetsa pa misanje ya dziko lapansi,
Ndipo anadya zipatso za m'minda;
Namyamwitsa uci wa m'thanthwe,
Ndi mafutam'mwala wansangalabwe;

14Mafuta a mkaka wang'ombe, ndi mkaka wankhosa,
Ndi mafuta a ana a nkhosa,
Ndi nkhosa zamphongo za mtundu wa ku Basana, ndi atonde,
Ndi imso zonenepa zatirigu;
Ndipo munamwa vinyo, mwazi wamphesa,
15Koma Yesuruni anasanduka wonenepa, natazira;
Wasanduka wonenepa, wakula, wakuta ndi mafuta;
Pamenepo anasiya Mulungu amene anamlenga,
Napeputsa thanthwe la cipulumutso cace.
16Anamcititsa nsanje ndi milungu yacilendo,
Anautsa mkwiyo wace ndi zonyansa.
17Anaziphera nsembe ziwanda, si ndizo Mulungu ai;
Milungu yosadziwa iwo,
Yatsopano yofuma pafupi, Imene makolo anu sanaiopa,
18Mwaleka Thanthwe limene linakubalani,
Mwaiwala Mulungu amene anakulengani.
19Ndipo Yehova anaciona, nawanyoza,
Pakuipidwa nao ana ace amuna, ndi akazi.
20Ndipo iye anati, Ndidzawabisira nkhope yanga,
Ndidzaona kutsiriza kwao;
Popeza iwo ndiwo mbadwo wopulukira,
Ana osakhulupirika iwo.
21Anautsa nsanje yanga ndi cinthu cosati Mulungu;
Anautsa mkwiyo wanga om zopanda pace zao.
Ndidzautsa nsanje yao ndi iwo osakhala mtundu wa anthu;
Ndidzautsa mkwiyo wao ndi mtundu wa anthu opusa.
22Pakuti wayaka moto mu mkwiyo wanga,
Utentha kumanda kunsi
Ukutha dziko lapansi ndi zipatso zace
Nuyatsa maziko a mapiri,
23Ndidzawaunjikira zoipa;
Ndidzawathera nubvi yanga.
24Adzaonda nayo njala
Adzanyekeka ndi makala a moto, cionongeko cowawa;
Ndipo ndidzawatumizira mana a zirombo,
Ndi ululu wa zokwawa m'pfumbi.
25Pabwalo lupanga lidzalanda,
Ndi m'zipinda mantha;
Lidzaononga mnyamata ndi namwali,
Woyamwa pamodzi ndi munthu waimvi.
26Ndinati, Ndikadawauzira ndithu,
Ndikadafafaniza cikumbukiro cao mwa anthu;
27Ndikadapanda kuopa mkwiyo wapamdani,
Angayese molakwa outsana nao,

Anganene, Lakwezeka dzanja lathu,
Ndipo Yehova sanacita ici conse.
28Popeza iwo ndiwo mtundu wa anthu wosowa uphungu konse,
Ndipo alibe cidziwitso.
29Akadakhala nazo nzeru, akadazindikira ici,
Akadasamalira citsirizo cao!
30Mmodzi akadapitikitsa zikwi,
Awiri akadathawitsa zikwi khumi,
Akadapanda kuwagulitsa Thanthwelao,
Akadapanda kuwapereka Yehova.
31Popeza thanthwe lao nlosanga Thanthwe lathu,
Oweruza a pamenepo ndiwo adani athu.
32Pakuti mpesa wao ndiwo wa ku Sodomu,
Ndi wa m'minda ya ku Gomora;
Mphesa zao ndizo mphesa zandulu,
Matsangwi ao ngowawa.
33Vinyo wao ndiwo ululu wa zinjoka,
Ndi ululu waukali wa mphiri.
34Kodi sicisungika ndi Ine,
Colembedwa cizindikilo mwa cuma canga ceni ceni?
35Kubwezera cilango nkwanga, kubwezera komwe,
Pa nyengo ya kuterereka phazi lao;
Pakuti tsiku la tsoka lao layandika,
Ndi zinthu zowakonzeratu zifulomira kudza.
36Popeza Yehova adzaweruza anthuace,
Nadzacitira nsoni anthu ace;
Pakuona iye kuti mphamvu yao yatha,
Wosatsala womangika kapena waufulu,
37Pamenepo adzati, Iri kuti milunguyao,
Thanthwe limene anathawirako?
38Imene inadya mafuta a nsembe zao zophera,
Nimwa vinyo wa nsembe yao yothira?
Iuke nikuthandizeni, Ikhale pobisalapo panu.
39Tapenyani tsopano kuti Ine ndine iye,
Ndipo palibe mulungu koma Ine;
Ndipha Ine, ndikhalitsanso ndi mayo:
Ndikantha, ndicizanso Ine;
Ndipo palibe wakulanditsa m'dzanja langa.
40Pakuti ndikweza dzanja langa kuloza kumwamba,
Ndipo nditi, Pali moyo wanga kosatha,
41Ndikanola lupanga langa lonyezimira,
Ndi dzanja langa likagwira ciweruzo;
Ndidzabwezera cilango ondiukira,
Ndi kulanga ondida.

42Mibvi yanga ndiiledzeretsa nao mwazi,
Ndi lupanga langa lidzalusira nyama;
Ndi mwazi wa ophedwa ndi ogwidwa,
Ndi mutu wacitsitsi wa mdani,
43Kondwerani, amitundu inu, ndi anthu ace;
Adzalipsira mwazi wa atumiki ace,
Adzabwezera cilango akumuukira,
Nadzafafanizira zoipa dziko lace, ndi anthu ace.
44Ndipo anadza Mose nanena mau onse a nyimbo iyi m'makutu mwa anthu, iye, ndi Hoseya mwana wa Nuni. 45Ndipo Mose anatha kunena mau awa onse kwa Israyeli wonse; 46nati nao, Ikani mitima yanu pa mau onse ndikucitirani nao mboni lero; kuti muuze ana anu asamalire kuwacita mau onse a cilamulo ici. 47Pakuti sicikhala kwa inu cinthu copanda pace, popeza ndico moyo wanu, ndipo mwa cinthu ici mudzacurukitsa masiku anu m'dziko limene muolokera Yordano, kulilandira.

Mulungu auza Mose akwere m'phiri la Nebo

48Ndipo Yehova ananena ndi Mose tsiku lomweli, ndi kuti, 49Kwera m'phiri muno mwa Abarimu, phiri la Nebo, lokhala m'dziko la Moabu, popenyana ndi Yeriko; nupenye dziko la Kanani, limene ndipereka kwa ana a Israyeli likhale lao lao; 50nufe m'phiri m'mene ukweramo, nuitanidwe kumka kwa anthu a mtundu wako; monga Aroni mbale wako anafa m'phiri la Hori, naitanidwa kumka kwa anthu a mtundu wace; 51popeza munandilakwira pakati pa ana a Israyeli ku madzi a Meriba wa Kadesi m'cipululu ca Zini, popeza simunandipatula Ine pakati pa ana a Israyeli, 52Pakuti udzapenya dzikoli pandunji pako; koma osalowako ku dziko limene ndipatsa ana a Israyeli.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Mose adalitsa mafuko 12 a Israyeli asanafe

1Ndipo mdalitso, Mose munthu wa Mulungu anadalitsa nao ana a
Israyeli asanafe, ndi uwu. 2Ndipo anati,
Yehova anafuma ku Sinai,
Nawaturukiraku Seiri;
Anaoneka wowala pa phiri la Parana,
Anafumira kwa opatulika zikwi zikwi;
Ku dzanja lamanja lace kudawakhalira lamulo lamoto.
3Inde akonda mitundu ya anthu;
Opatulidwa ace onse ali m'dzanjamwanu;
Ndipo akhala pansi ku mapazi anu;
Yense adzalandirako mau anu.
4Mose anatiuza cilamulo,
Colowa ca msonkhano wa Yakobo.
5Ndipo iye anali mfumu m'Yesuruni,
Pakusonkhana mafumu a anthu,
Pamodzi ndi mapfuko a Israyeli.
6Rubeni akhale ndi moyo, asafe,
Koma amuna ace akhale owerengeka.
7Za Yuda ndi izi; ndipo anati,
Imvani, Yehova, mau a Yuda,
Ndipo mumfikitse kwa anthu ace;
Manja ace amfikire;
Ndipo mukhale inu thandizo lace pa iwo akumuukira.
8Ndipo za Levi anati,
Tumimu ndi Urimu wanu zikhala ndi wokondedwa wanu,
Amene mudamuyesa m'Masa,
Amene mudalimbana naye ku madzi a Meriba;
9Amene anati za atate wace ndi amai wace, Sindinamuone;
Sanazindikira abale ace,
Sanadziwa ana ace omwe;
Popeza anasamalira mau anu, Nasunga cipangano canu.
10Adzaphunzitsa Yakobo maweruzo anu,
Ndi Israyeli cilamulo canu;
Adzaika cofukiza pamaso panu,
Ndi nsembe yopsereza yamphumphu pa guwa la nsembe lanu.
11Dalitsani, Yehova, mphamvu yace,
Nimulandire nchito ya manja ace;
Akantheni m'cuuno iwo akumuukira,
Ndi iwo akumuda, kuti asaukenso.
12Za Benjamini anati,
Wokondedwa wa Yehova adzakhala ndi iye mokhazikika;
Amphimba tsiku lonse,

Inde akhalitsa pakati pa mapewa ace.
13Ndipo za Yosefe anati,
Yehova adalitse dziko lace;
Ndi zinthu zofunikatu za m'mwamba, ndi mame,
Ndi madzi okhala pansipo;
14Ndi zipatso zofunikatu za dzuwa,
Ndi zomera zofunikatu za mwezi,
15Ndi zinthu zoposa za mapiri akale,
Ndi zinthu zofunikatu za zitunda zosatha,
16Ndi zinthu zofunikatu za dziko lapansi, ndi kudzala kwace,
Ndi cibvomerezo ca iye anakhala m'citsambayo;
Mdalitso ufike pa mutu wa Yosefe,
Ndi pakati pa mutu wace wa iye wokhala padera ndi abale ace.
17Woyamba kubadwa wa ng'ombe yace, ulemerero ndi wace;
Nyanga zace ndizo nyanga zanjati;
Adzatunga nazo mitundu ya anthu pamodzi, kufikira malekezero a dziko lapansi.
Iwo ndiwo zikwi khumi za Efraimu,
Iwo ndiwo zikwi za Manase.
18Ndi za Zebuloni anati,
Kondwera, Zebuloni, ndi kuturukakwako;
Ndi Isakara, m'mahema mwako.
19Adzaitana mitundu ya anthu afike kuphiri;
Apo adzaphera nsembe za cilungamo;
Popeza adzayamwa zocuruka za m'nyanja,
Ndi cuma cobisika mumcenga.
20Ndi za Gadi anati,
Wodala iye amene akuza Gadi;
Akhala ngati mkango waukazi,
Namwetula dzanja, ndi pakati pa mutu pomwe.
21Ndipo anadzisankhira gawo loyamba,
Popeza kumeneko kudasungika gawo la wolamulira;
Ndipo anadza ndi mafumu a anthu,
Anacita cilungamo ca Yehova,
Ndi maweruzo ace ndi Israyeli.
22Ndi za Dani anati,
Dani ndiye mwana wa mkango,
Wakutumpha moturuka m'Basana.
23Za Nafitali anati,
Nafitali, wokhuta nazo zomkondweretsa,
Wodzala ndi mdalitso wa Yehova;
Landira kumadzulo ndi kumwela.
24Ndi za Aseri anati,
Aseri adalitsidwe mwa anawo;

Akhale wobvomerezeka mwa abale ace,
Abviike phazi lace m'mafuta.
25Nsapato zako zikhale za citsulo ndi mkuwa;
Ndipo monga masiku ako momwemo mphamvu yako.
26Palibe wina ngati Mulungu, Yesuruni iwe,
Wakuyenda wokwera pathambo, kukuthandiza,
Ndi pa mitambo m'ukulu wace.
27Mulungu wamuyaya ndiye mokhaliramo mwako;
Ndi pansipo pali manja osatha.
Ndipo aingitsa mdani pamaso pako,
Nati, Ononga.
28Ndipo Israyeli akhala mokhazikika pa yekha;
Kasupe wa Yakobo;
Akhala m'dziko la tirigu ndi vinyo;
Inde thambo lace likukha mame.
29Wodala iwe, Israyeli;
Akunga iwe ndani, mtundu wa anthu opulumutsidwa ndi Yehova,
Ndiye cikopa ca thandizo lako,
Iye amene akhala lupanga la ukulu wako!
Ndi adani ako adzakugonjera; Ndipo udzaponda pa misanje yao.

©The Bible Society of Malawi, 1992

1Ndipo Mose anakwera kucokera ku zidikha za Moabu, kumka ku
phiri la Nebo, pamwamba pa Pisiga, popenyana ndi Yeriko. Ndipo
Yehova anamuonetsa dziko lonse la Gileadi, kufikira ku Dani; 2ndi
Nafitali lonse, ndi dziko la Efraimu, ndi Manase, ndi dziko lonse la
Yuda, kufikira nyanja ya m'tsogolo; 3ndi kumwela, ndi cidikha eli
cigwa ca Yeriko, mudzi wa migwalangwa, kufikira ku Zoari. 4Ndipo
Yehova anati kwa iye, Si ili dziko ndinalumbirira Abrahamu, Isake,
ndi Yakobo, ndi kuti, Ndidzalipereka kwa mbeu zako. Ndinakuonetsa
ili m'maso, koma sudzaolokako. 5Ndipo Mose mtumiki wa Yehova
anamwalirako m'dziko la Moabu, monga mwa mau a Yehova. 6Ndipo
iye anamuika m'cigwa m'dziko la Moabu popenyana ndi Beti-peori;
koma palibe munthu wakudziwa kumanda kwace kufikira lero
lino. 7Ndipo zaka zace za Mose ndizo zana limodzi ndi makumi awiri,
pakumwalira iye; diso lace silinacita mdima, ndi mphamvu yace
siidaleka. 8Ndipo ana a Israyeli analira Mose m'zidikha za Moabu
masiku makumi atatu; potero anatha masiku akulira maliro a
Mose. 9Ndipo Yoswa mwana wa Nuni anadzala ndi mzimu wanzeru;
popeza Mose adamuikira manja ace; ndi ana a Israyeli anamvera
iye, nacita monga Yehova adauza Mose. 10Ndipo sanaukanso
mnereri m'Israyeli ngati Mose, amene Yehova anadziwana naye
popenyana maso; 11kunena za zizindikilo ndi zozizwa zonse zimene
Yehova anamtumiza kuzicita m'dziko la Aigupto kwa Farao, ndi
anyamata ace onse, ndi dziko lace lonse; 12ndi kunena za dzanja la
mphamvu lonse, ndi coopsa cacikuru conse, cimene Mose anacita
pamaso pa Israyeli wonse.
©The Bible Society of Malawi, 1992

Joshua

Yoswa 1

1NDIPO atafa Mose mtumiki wa Yehova, Yehova anati kwa Yoswa
mwana wa Nuni mnyamata wa Mose, 2Mose mtumiki wanga wafa;
tauka tsono, nuoloke Yordano uyu, iwe ndi anthu awa onse, kulowa
m'dzikomo ndirikuwapatsa, ndiwo ana a Israyeli. 3Pali ponse phazi
lanu lidzapondapo ndinakupatsani, monga ndinanena ndi
Mose. 4Kuyambira cipululu, ndi Lebano uyu, kufikira mtsinje
waukulu mtsinje wa Firate, dziko lonse la Ahiti, ndi kufikira nyanja
yaikuru ku malowero a dzuwa, ndiwo malire anu. 5Palibe munthu
adzatha kuima pamaso pako masiku onse a moyo wako; monga
ndinakhala ndi Mose momwemo ndidzakhala ndi iwe;
sindidzakusowa, sindidzakusiya. 6Khala wamphamvu, nulimbike
mtima, pakuti udzagawira anthu awa dzikoli likhale colowa cao,
ndilo limene ndinalumbirira makolo ao kuwapatsa. 7Komatu khala
wamphamvu, nulimbike mtima kwambiri, kuti usamalire kucita
monga mwa cilamulo conse anakulamuliraco Mose mtumiki wanga;
usacipambukire ku dzanja lamanja kapena kulamanzere, kuti
ukacite mwanzeru kuli konse umukako. 8Buku ili la cilamulo lisacoke
pakamwa pako; koma ulingiriremo usana ndi usiku, kuti usamalire
kucita monga mwa zonse zolembedwamo; popeza ukatero
udzakometsa njira yako, nudzacita mwanzeru. 9Kodi
sindinakulamulira iwe? Khala wamphamvu, nulimbike mtima,
usaope, kapena kutenga nkhawa, pakuti Yehova Mulungu wako ali
ndi iwe kuli konse umukako.
10Pamenepo Yoswa analamulira akapitao a anthu, ndi kuti, 11Pitani
pakati pa cigono, nimulamulire anthu, ndi kuti, Mudzikonzeretu
kamba, pakuti asanapite masiku atatu mudzaoloka Yordano uyu,
kulowa ndi kulandira dziko limene Yehova Mulungu wanu
akupatsani, likhale lanu lanu.
12Ndipo Yoswa anati kwa Arubeni, ndi Agadi, ndi pfuko la Manase
logawika pakati, ndi kuti, 13Kumbukilani mau amene Mose mtumiki
wa Yehova anakulamulirani inu, kuti, Yehova Mulungu wanu
akupatsani mpumulo, nadzakupatsani dziko lino. 14Akazi anu, ana
anu, ndi zoweta zanu zikhale m'dzikoli anakuninkhani Mose, tsidya
lino la Yordano; koma inu muoloke okonzeka kunkhondo pamaso pa
abale anu, ngwazi zonse, ndi kuwathandiza; 15mpaka Yehova
atapatsa abale anu mpumulo, monga umo anakuninkhirani inu,
naonso alandira dzikolo awaninkha Yehova Mulungu wanu;
pamenepo mubwerere ku dziko lanu lanu, ndi kukhala nalo, limene
Mose mtumiki wa Yehova anakupatsani tsidya lino la Yordano la
kum'mawa, 16Ndipo anamyankha Yoswa, nati, Zonse mwatilamulira
tidzacita, ndipo kuli konse mutitumako tidzamuka. 17Monga

momwe tinamvera mau onse a Mose momwemo tidzamvera inu;
komatu akhale ndi inu Yehova Mulungu wanu monga anakhala ndi
Mose. 18Ali yense wakupikisana ndi inu, osamvera mau anu muli
monse mukamlamulira, aphedwe; komatu khalani wamphamvu,
nimulimbike mtima.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Yoswa atuma anthu awiri azonde Yeriko

1Ndipo Yoswa mwana wa Nuni, ali ku Sitimu, anatuma amuna awiri
mosadziwika kukazonda, ndi kuti, Mukani, mulipenye dzikolo, ndi
ku Yeriko. Ndipo anamuka nalowa m'nyumba ya mkazi wadama,
dzina lace Rahabi, nagona momwemo. 2Ndipo wina anaiuza mfumu
ya Yeriko, kuti, Taonani, usiku uno alowa muno amuna a ana a
Israyeli, kulizonda dziko. 3Ndipo mfumu ya Yeriko inatuma wina
kwa Rahabi, ndi kuti, Turutsa amunawo anafika kwanu, amene
analowa m'nyumba mwako; popeza anadzera kulizonda dziko
lonse. 4Koma mkaziyo anatenga amuna awiriwo, nawabisa; natero,
Inde, amunawo anandifikira; koma sindinadziwa uko afuma; 5ndipo
m'mene akadati atseke pacipata, kutada, anaturuka amunawo; uko
anamuka amunawo osakudziwa ine; muwalondole msanga, pakuti
mudzawapeza. 6Koma adawakweretsa patsindwi, nawabisa ndi
mitengo yanthamza yoyanika patsindwi. 7Ndipo amunawo
anawalondola pa njira ya ku Yordano yomka kudooko; ndipo
ataturuka akuwalondola, anatseka pacipata. 8Koma asanagone
iwo, anawakwerera patsindwi iye, 9nati kwa amunawo, Ndidziwa
kuti Yehova wakupatsani dzikoli, ndi kuti kuopsa kwanu
kwatigwera, ndi kuti okhala m'dziko onse asungunuka pamaso
panu. 10Popeza tidamva kuti Yehova anaphwetsa madzi a m'Nyanja
Yofiira pamaso panu, muja mudaruruka m'Aigupto; ndi cija
munacitira mafumu awiri a Aamori okhala tsidya la Yordano, ndiwo
Sihoni ndi Ogi, amene mudawaononga konse. 11Ndipo titamva ici
mitima yathu inasungunuka; anahbenso mtima ndi mmodzi yense,
cifukwa ca inu; pakuti Yehova Mulungu wanu, ndiye Mulungu wa
m'mwamba umo, ndi pa dziko lapansi. 12Ndipo tsopano,
mundilumbiriretu kwa Yehova, popeza ndakucitirani cifundo, kuti
inunso mudzacitira cifundo a m'nyumba ya atate wanga ndi
kundipatsa cizindikilo coona, 13kuti mudzawasunga ndi moyo atate
wanga ndi mai wanga, ndi alongo anga ndi abale anga, ndi zonse
ali nazo, ndi kupulumutsa miyoyo yathu kuimfa. 14Ndipo amunawo
anati kwa iye, Moyo wathu ndiwo moyo wanu, mukapanda kuulula
codzera ife; ndipo kudzakhala kuti, pakutipatsa ife dziko ili Yehova,
tidzakucitira cifundo ndi coonadi. 15Pamenepo anawatsitsa
pazenera ndi cingwe; popeza nyumba yace lnali pa linga La mudzi,
nakhala iye palingapo. 16Ndipo anati kwa iwo, Mukani kuphiri,
olondola angakupezeni; mubisale kumeneko masiku atatu, mpaka
atabwerera olondolawo, pamenepo muyende ulendo
wanu. 17Ndipo amunawo anati kwa iye, Sitidzacimwira lumbiro lako
ili watilumbiritsali. 18Taona, tikadzalowa m'dzikomo ife, uzimanga
cingwe ici cofiira pazenera pamene watitsitsira; ndipo
udzasonkhanitsa m'nyumbamo atate wako ndi mai wako nui abale

ako ndi a m'nyumba onse a atate wako. 19Ndipo kudzakhala kuti ali
yense akadzaturuka pa khomo la nyumba yako kubwalo, imfa
imeneyi ndi yace, tiribe kuparamula ife; koma ali yense adzakhala
ndi iwe m'nyumba, likamfikira dzanja, imfa imeneyi ndi
yathu. 20Koma ukaulula codzera ifeco tidzamasukira lumbiro lako
watilumbiritsali. 21Nati iye, Momwemo, monga mwa mau anu.
Ndipo anawauza amuke, iwo namuka; namanga iye cingwe
cofiiraco pazenera. 22Ndipo anayenda iwo, nafika kuphiri,
nakhalako masiku atatu mpaka atabwerera olondolawo; popeza
olondolawo anawafunafuna panjira ponse,
osawapeza. 23Pamenepo amuna awiriwo anabwerera, natsika
m'phirimo naoloka, nafika kwa Yoswa mwana wa Nuni,
namfotokozera zonse zidawagwera. 24Ndipo anati kwa Yoswa,
Zoonadi, Yehova wapereka dziko lonse m'manja mwathu; ndiponso
nzika zonse zasungunuka pamaso pathu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Aisrayeli aoloka Yordano

1Ndipo Yoswa analawirira mamawa, kucoka ku Sitimu, nafika ku
Yordano, iye ndi ana onse a Israyeli; nagona komweko,
asanaoloke. 2Ndipo kunali atapita masiku atatu, akapitao anapita
pakati pa cigono; 3nalamulira anthu, ndi kuti, Mukadzaona likasa la
cipangano la Yehova Mulungu wanu, ndi ansembe Aleviwo
atalisenza, pamenepo mucoke kwanu ndi kulitsata. 4Koma pakhale
dera pakati pa inu ndi ilo, monga mikono zikwi ziwiri poliyesa;
musaliyandikire, kuti mudziwe njira imene muziyendamo; popeza
simunapita njirayi kufikira lero. 5Ndipo Yoswa ananena kwa anthu,
Mudzipatule, pakuti mawa Yehova adzacita zodabwiza pakati pa
inu. 6Ndipo Yoswa anati kwa ansembe, Senzani likasa la cipangano,
nimuoloke pamaso pa anthu. Nasenza iwo likasa la cipangano,
natsogolera anthu. 7Ndipo Yehova anati kwa Yoswa, Lero lino
ndidzayamba kukukuza pamaso pa Aisrayeli onse, kuti adziwe, kuti
monga momwe ndinakhalira ndi Mose, momwemo ndidzakhala ndi
iwe. 8Ndipo uzilamulira ansembe akunyamula likasa la cipangano,
ndi kuti, Pamene mufika kumphepete kwa madzi a Yordano
muziima m'Yordano.
9Ndipo Yoswa anati kwa ana a Israyeli, Idzani kuno, mumve mau a
Yehova Molungu wanu. 10Nati Yoswa, Ndi ici mudzadziwa kuti
Mulungu wamoyo ali pakati pa inu, ndi kuti adzapitikitsa ndithu
pamaso panu Akanani, ndi Ahiti, ndi Ahivi, ndi Aperizi, ndi
Agirigasi, ndi Aamori, ndi Ayebusi. 11Taonani, likasa la cipangano
La Ambuye wa dziko lonse lapansi lioloka Yordano pamaso
panu, 12Ndipo tsono, mudzitengere amuna khumi ndi awiri mwa
mapfuko a Israyeli, pfuko limodzi mwamuna mmodzi. 13Ndipo
kudzakhala, akaima mapazi a ansembe akusenza likasa la Yehova
Ambuye wa dziko lonse, m'madzi a Yordano, adzadulidwa
madziwo, ndiwo madzi ocokera kumagwero, nadzaima mulu
umodzi. 14Ndipo kunali pocoka anthu ku mahema ao kukaoloka
Yordano, ansembe anasenza likasa la cipangano pamaso pa
anthu. 15Ndipo pamene iwo akusenza likasa anafika ku Yordano,
nathibika m'mphepete mwa madzi mapazi a ansembe akusenza
likasa, pakuti Yordano asefuka m'magombe ace onse, nyengo
yonse ya masika, 16pamenepo madzi ocokera kumagwero anaima,
nauka ngati mulu, kutalitu ku Adamu, ndiwo mudzi wa ku mbali ya
Zaretani; koma madzi akutsikira kumka ku nyanja ya cidikha, ndiyo
Nyanja ya Mcere, anadulidwa konse; ndipo anthu anaoloka
pandunji pa Yeriko. 17Ndipo ansembe akulisenza likasa la
cipangano la Yehova, anaima pouma pakati pa Yordano, ndi
Aisrayeli onse anaoloka pouma mpaka mtundu wonse unatha
kuoloka Yordano.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Aimiritsa miyala 12 ikhale cikumbutso ku Giligala

1Ndipo kunali, utatha kuoloka Yordano mtundu wonse, Yehova
ananena ndi Yoswa, nati, 2Mudzitengere mwa anthu, amuna khumi
ndi awiri, pfuko limodzi mwamuna mmodzi; 3ndipo muwalamulire
iwo ndi kuti, Mudzitengere pano pakati pa Yordano, poimapo
mapazi a ansembe, miyala khumi ndi iwiri, ndi kuoloka nayo, ndi
kulika m'mogona m'mene mugonamo usiku uno. 4Pamenepo Yoswa
anaitana amuna khumi ndi awiriwo amene anawaikiratu mwa ana
a Israyeli, pfuko limodzi mwamuna mmodzi; 5nanena nao Yoswa,
Olokani, kutsogolera likasa la Yehova Mulungu wanu pakati pa
Yordano, nimudzisenzere yense mwala paphewa pace, monga mwa
kuwerenga kwa mapfuko a ana a Israyeli; 6kuti ici cikhale
cizindikilo pakati pa inu. Akakufunsani ana anu m'tsogolomo, ndi
kuti, Miyala iyi nja ciani ndi inu? 7munene nao, Cifukwa madzi a
Yordano anadulidwa patsogolo pa likasa la cipangano ca Yehova;
muja lidaoloka Yordano, madzi a Yordano anadulidwa; ndipo miyala
iyi idzakhala cikumbutso ca ana a Israyeli cikhalire. 8Ndipo ana a
Israyeli anacita monga Yoswa anawalamulira, nasenza miyala
khumi ndi iwiri pakati pa Yordano, monga Yehova adalankhula ndi
Yoswa, monga mwa kuwerenga kwa mapfuko a ana a Israyeli;
ndipo anaoloka nayo kumka kogona, naiika komweko. 9Ndipo
Yoswa anaimika miyala khumi ndi iwiri pakati pa Yordano, poimapo
mapazi a ansembe akusenza likasa la cipangano; ikhala komweko
kufikira lero lino. 10Pakuti ansembe akusenza likasa anaima pakati
pa Yordano, mpaka zitatha zonse Yehova adazilamulira Yoswa
anene kwa anthu, monga mwa zonse Mose adalamulira Yoswa;
ndipo anthu anafulumira kuoloka. 11Ndipo kunali, atatha kuoloka
anthu onse, likasa la Yehova linaoloka, ndi ansembe, pamaso pa
anthu. 12Ndipo ana a Rubeni, ndi ana a Gadi, ndi gawo lija la pfuko
la Manase anaoloka ndi zida zao pamaso pa ana a Israyeli, monga
Mose adanena nao; 13ngati zikwi makumi anai ankhondo okonzeka
anaoloka pamaso pa Yehova kuthira nkhondo ku zidikha za
Yeriko. 14Tsiku lomwelo Yehova anakulitsa Yoswa pamaso pa
Aisrayeli onse; ndipo anamuopa monga anaopa Mose, masiku onse
amoyowace.
15Ndipo Yehova anati kwa Yoswa, 16Lamulira ansembe akusenza
likasa la umboni, kuti akwere kuturuka m'Yordano. 17Pamenepo
Yoswa analamulira ansembe, ndi kuti, Kwerani kuturuka
m'Yordano. 18Ndipo kunali, atakwera ansembe akusenza likasa la
cipangano la Yehova, kuturuka pakati pa Yordano, nakwera
pamtunda mapazi a ansembe, madzi a m'Yordano anabwera
m'njira mwace, nasefuka m'magombe ace onse monga
kale. 19Ndipo anthu anakwera kuturuka m'Yordano tsiku lakhumi la

mwezi woyamba, namanga misasa ku Giligala, mbali ya ku
m'mawa kwa Yeriko. 20Ndipo Yoswa anaimika ku Giligala miyala ija
khumi ndi iwiri adaitenga m'Yordano. 21Ndipo anati kwa ana a
Israyeli, Ana anu akadzafunsa atate ao masiku akudza, ndi kuti,
Miyala iyi nja ciani? 22pamenepo muzidziwitsa ana anu, ndi kuti,
Israyeli anaoloka Yordano uyu pouma. 23Pakuti Yehova Mulungu
wanu anaphwetsa madzi a Yordano pamaso panu, mpaka
mutaoloka; monga Yehova Mulungu wanu anacitira Nyanja Yofiira,
imene anaiphwetsa pamaso pathu, mpaka titaoloka; 24kuti
mitundu yonse ya pa dziko lapansi idziwe dzanja la Yehova, kuti
ndilo lamphamvu; kuti lope Yehova Mulungu wanu masiku onse.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Anthu adulidwa nacita Paskha

1Ndipo kunali, pamene mafumu onse a Aamori okhala tsidya la
kumadzulo la Yordano, ndi mafumu onse a Akanani okhala ku
Nyanja ya Mcere anamvakuti Yehova anaphwetsa madzi a Yordano
pamaso pa ana a Israyeli mpaka titaoloka, mtima wao
unasungunuka, analibenso moyo cifukwa ca ana a Israyeli. 2Nthawi
imeneyo Yehova anati kwa Yoswa, Udzisemere mipeni yamiyala,
nudulenso ana a Israyeli kaciwiri. 3Ndipo Yoswa anadzisemera
mipeni yamiyala nadula ana a Israyeli pa Gibeya Naraloti. 4Koma
cifukwa cakuti Yoswa anawadula ndi ici: anthu onse oturuka
m'Aigupto, anthu amuna, ndiwo amuna onse ankhondo, adafa
m'cipululu panjira, ataturuka m'Aigupto. 5Pakuti anthu onse
anaturukawo anadulidwa; koma anthu onse obadwa m'cipululu
panjira poturuka m'Aigupto sanadulidwa. 6Pakuti ana a Israyeli
anayenda m'cipululu zaka makumi anai, mpaka mtundu wonse wa
amuna ankhondo oturuka m'Aigupto udatha, cifukwa ca
kusamvera mau a Yehova; ndiwo amene Yehova anawalumbirira
kuti sadzawaonetsa dziko limene Yehova analumbirira makolo ao
kudzatipatsa, ndilo dziko moyenda mkaka ndi uci. 7Koma ana ao
amuna amene anawautsa m'malo mwao, iwowa Yoswa anawadula;
popeza anakhala osadulidwa, pakuti sanawadula panjira. 8Ndipo
kunali, atatha kudula mtundu wonse, anakhala m'malo mwao
m'cigono mpaka adacira. 9Ndipo Yehova anati kwa Yoswa, Lero Uno
ndakukunkhunizirani mtonzo wa Aigupto, Cifukwa cace dzina la
malowo analicha Giligala kufikira lero lino.
10Ndipo ana a Israyeli anamanga misasa ku Giligala; nacita Paskha
tsiku lakhumi ndi cinai la mwezi, madzulo, m'zidikha za
Yeriko. 11Ndipo m'mawa mwace atatha Paskha, anadya tirigu
wakhwimbi wa m'dziko, mikate yopanda cotupitsa ndi tirigu
wokazinga tsiku lomwe lija. 12Koma m'mawa mwace mana
analeka, atadya iwo tirigu wakhwimbi wa m'dziko; ndipo ana a
Israyeli analibenso mana; koma anadya zipatso za dziko la Kanani
caka comwe cija.

Masomphenya a Yoswa

13Ndipo kunali, pokhala Yoswa ku Yeriko, anakweza maso ace,
napenya, ndipo taona, panaima muthu pandunji pace ndi lupanga
lace losolola m'dzanja lace; namuka Yoswa kuli iye, nati iye,
Ubvomerezana ndi ife kapena ndi aelani athu? 14Nati, lai, koma
ndadza ine, kazembe wa ankhondo a Yehova. Pamenepo Yoswa
anagwa nkhope yace pansi, napembedza, nati kwa iye, Anenanji
Ambuyanga kwa mtumiki wace? 15Ndipo kazembe wa ankhondo a
Yehova anati kwa Yoswa, Bvula nsapato yako pa phazi lako; pakuti
malo upondapo mpopatulika. Nacita Yoswa comweco.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Kupasulidwa kwa Yeriko

1Koma ku Yeriko anatseka pazipata, natsekedwa cifukwa ca ana a
Israyeli, panalibe woturuka, panalibenso wolowa. 2Ndipo Yehova
ananena kwa Yoswa, Taona, ndapereka m'dzanja lako Yeriko ndi
mfumu yace, ndi ngwazi zace. 3Ndipo muzizungulira mudzi Inu
nonse ankhondo, kuuzungulira mudzi kamodzi. Muzitero masiku
asanu ndi limodzi. 4Ndipo ansembe asanu ndi awiri azinyamula
mphalasa zisanu ndi ziwiri zanyanga: za nkhosa zamphongo,
natsogolere nazo likasa; koma tsiku lacisanu ndi ciwiri
muzizungulira mudziwo kasanu ndi kawirio ndi ansembe aziliza
mphalasazo. 5Ndipo kudzakhala kuti akaliza cilizire ndi nyanga ya
nkhosa yamphongo, nimumva kulira kwa mphalasa, anthu onse
apfuule mpfuu yaikuru; ndipo linga la mudziwo lidzagwa pomwepo,
ndi anthu adzakwera ndi kulowamo yense kumaso kwace. 6Ndipo
Yoswa mwana wa Nuni anaitana ansembe, nanena nao, Senzani
likasa la cipangano, ndi ansembe asanu ndi awiri anyamule
mphalasa zisanu ndi ziwiri zanyanga za nkhosa zamphongo,
kutsogolera nazo likasa la Yehova. 7Nati kwa anthu, Pitani,
muzizungulira mudzi, ndi ankhondo ndi zida zao atsogolere likasa
la Yehova. 8Ndipo atanena kwa anthu Yoswa, ansembe asanu ndi
awiri akunyamula mphalasa zisanu ndi ziwiri zanyanga za nkhosa
zamphongo pamaso pa Yehova, anapita naliza mphalasazo; ndipo
likasa la cipangano ca Yehova linawatsata. 9Ndipo okonzeka
kunkhondo anatsogolera ansembe akuliza mphalasa, koma akudza
m'mbuyo anatsata likasa, ansembe ali ciombere poyenda
iwo. 10Ndipo Yoswa analamulira anthu, ndi kuti, Musamapfuula,
kapena kumveketsa mau anu, asaturuke konse mau m'kamwa
mwanu, mpaka tsiku lakunena nanu ine, Pfuulani; pamenepo
muzipfuula. 11Ndipo anazungulitsa likasa la Yehova mudzi,
kuzungulira kamodzi; pamenepo analowa kucigono, nagona
m'mwemo.
12Ndipo Yoswa analawira mamawa, ndi ansembe anasenza likasa
la Yehova. 13Ndipo ansembe asanu ndi awiri, akunyamula
mphalasa zisanu ndi ziwiri zanyanga za nkhosa zamphongo ndi
kutsogolera nazo likasa la Yehova, anayenda ciyendere naliza
mphalasazo; ndi okonzeka kunkhondowo anawatsogolera, ndi
akudza m'mbuyo anatsata likasa la Yehova, ansembe ali ciombere
poyenda iwo. 14Ndipo tsiku laciwiri anazungulira mudzi kamodzi,
nabwera kucigono; anatero masiku asanu ndi limodzi. 15Ndipo
kunali, tsiku lacisanu ndi ciwiri analawira mamawa, mbandakuca,
nazungulira mudzi mommuja kasanu ndi kawiri; koma tsiku lijalo
anazungulira mudzi kasanu ndi kawiri. 16Ndipo kunali, pa nthawi
yacisanu ndi ciwiri, pamene ansembe analiza mphalasa, Yoswa

anati kwa anthu, Pfuulani; pakuti Yehova wakupatsani mudziwo. 17Koma mudziwo udzaperekedwa kwa Yehova ndi kuonongeka konse, uwu ndi zonse ziri m'mwemo; Rahabi yekha wadamayo adzakhala ndi moyo, iye ndi onse ali naye m'nyumba, cifukwa anabisa mithenga tinawatumawo. 18Ndipo inu, musakhudze coperekedwaco, mungadziononge konse, potapa coperekedwaco; ndi kuononga konse cigono ca Israyeli ndi kucisautsa. 19Koma siliva yense, ndi golidi yense, ndi zotengera za mkuwa ndi citsulo zikhala copatulikira Yehova; zilowe m'mosungira cuma ca Yehova. 20Ndipo anthu anapfuula, naliza mphalasa ansembe; ndipo kunali, pamene anthu anamva kulira kwa mphalasa, anapfuula anthu ndi mpfuu yaikuru, niligwa linga pomwepo; nakwera anthu kulowa m'mudzi, yense kumaso kwace; nalanda mudziwo.

Apulumutsidwa Rahabi

21Ndipo anapereka kuzionong a ndi lupanga lakuthwa zonse za m'mudzi, amuna ndi akazi omwe, ana ndi nkhalamba zomwe, kudza ng'ombe, ndi nkhosa, ndi aburu, ndi lupanga lakuthwa. 22Ndipo Yoswa ananena kwa amuna awiri anazonda dzikowo, Lowani m'nyumba ya mkazi wadamayo, ndi kuturutsamo mkaziyo ndi zonse ali nazo, monga munamlumbirira iye. 23Pamenepo anyamata ozondawo analowa, naturutsa Rahabi, ndi atate wace ndi mai wace ndi abale ace, ndi onse anali nao; anaturutsanso acibale ace onse; nawaika kunja kwa cigono ca Israyeli. 24Ndipo anatentha mudzi ndi moto, ndi zonse zinali m'mwemo; koma siliva ndi golidi ndi zotengera zamkuwa ndi zacitsulo anaziika m'mosungira cuma ca nyumba ya Yehova. 25Koma Rahabi, mkazi wadamayo ndi banja la atate wace, ndi onse anali nao, Yoswa anawasunga ndi moyo; ndipo anakhala pakati pa Israyeli mpaka lero tino; cifukwa anabisa mithenga imene Yoswa anaituma kuzonda Yeriko. 26Ndipo Yoswa anawalumbirira nyengo ija, ndi kuti, Wotembereredwa pamaso pa Yehova munthu amene adzauka ndi kumanga mudzi uwu wa Yeriko; adzamanga kuzika kwace ndi kutayapo mwana wace woyamba, nadzaimika zitseko zace ndi kutayapo mwana wace wotsirizira. 27Potero Yehova anakhala ndi Yoswa; ndi mbiri yace inabuka m'dziko lonse.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Kucimwa kwa Akani

1Koma ana a Israyeli analakwa ndi coperekedwaco; popeza Akani
mwana wa Karimi, mwana wa Zabidi, mwana wa Zera, wa pfuko la
Yuda, anatapa coperekedwaco; ndi mkwiyo wa Yehova unayakira
ana a Israyeli.
2Ndipo Yoswa anatuma amuna kucokera ku Yeriko apite ku Ai,
ndiwo pafupi pa Beti-aveni, kum'mawa kwa Beteli; nanena nao,
Kwerani ndi kukazonda dziko. Nakwera amunawo, nazonda
Ai. 3Ndipo anabwera kwa Yoswa, nati kwa iye, Asakwere anthu
onse; koma akwere amuna ngati zikwi ziwiri kapena zitatu
kukantha Ai; musalemetsa anthu onse kumkako, pakuti a komweko
ndi owerengeka; 4Potero mwa anthu anakwerako amuna monga
zikwi zitatu; koma anathawa pamaso pa amuna a ku Ai. 5Ndipo
amuna a ku Ai anawakantha amuna, ngati makumi atatu
mphambu asanu ndi mmodzi; nawapitikitsa kuyambira pacipata
mpaka ku Sebarimu, nawakantha potsika; ndi mitima ya anthu
inasungunuka inga madzi. 6Ndipo Yoswa anang'amba zobvala
zace, nagwa nkhope yace pansi, ku likasa la Yehova, mpaka
madzulo, iye ndi akulu akulu a Israyeli, nathira pfumbi pamitu
pao. 7Ndipo Yoswa anati, Ha! Ambuye, Yehova, mwaolotseranji
anthu awa pa Yordano, kutipereka ife m'dzanja la Aamori,
kutiononga ife? mwenzi titalola ndi kukhala tsidya lija la
Yordano! 8Ndidzanenanji, Ambuye, Israyeli atabwerera m'mbuyo
pamaso pa adani ao? 9Akadzamva ici Akanani ndi okhala m'dziko
onse, adzatizinga ndi kuduliratu dzina lathu pa dziko lapansi; ndipo
mudzacitiranji dzina lanu lalikuru? 10Ndipo Yehova anati kwa
Yoswa, Tauka, wagweranji pankhope pako cotere? 11Israyeli
wacimwa, nalakwiranso cipangano canga, ndinawalamuliraco;
natengakonso coperekedwaco; anabanso, nanyenganso, naciika
pakati pa akatundu ao. 12Mwa ici ana a Israyeli sangathe kuima
pamaso pa adani ao, awafulatira adani ao, pakuti aperekedwa
aonongeke. Sindidzakhalanso nanu mukapanda kuononga
coperekedwaco, kucicotsa pakati pa inu. 13Tauka, patula anthu,
nuti, Mudzipatulire mawa; pakuti atero Yehova Mulungu wa Israyeli,
Pali coperekedwa cionongeke pakati pako, Israyeli iwe; sukhoza
kuima pamaso pa adani ako, mpaka mutacotsa coperekedwaco
pakati panu. 14Koma m'mawa adzakuyandikitsani, pfuko ndi pfuko;
ndipo kudzali kuti pfukoli Yehova aliulula lidzayandikira mwa zibale
zace; ndi cibale Yehova aciulula cidzayandikira monga mwa a
nyumba ace; ndi a m'nyumbawo Yehova awaulula adzayandikira
mmodzi mmodzi. 15Ndipo kudzali kuti iye wogwidwa ali naco
coperekedwaco adzatenthedwa ndi moto, iye ndi zonse ali nazo

cifukwa analakwira cipangano ca Yehova, ndi cifukwa anacita copusa m'Israyeli.
16Ndipo Yoswa analawira mamawa, nayandikizitsa Israyeli, pfuko ndi pfuko; ndi pfuko la Yuda linagwidwa; 17nayandikizitsa zibale za Yuda, nagwira cibale ca Azari; nayandikizitsa cibale ca Azari, mmodzi mmodzi, nagwidwa Zabidi; 18nayandikizitsa a m'nyumba yace mmodzi mmodzi; ndipo Akani, mwana wa Karimu, mwanu wa Zabidi, mwana wa Zera, wa pfuko la Yuda anagwidwa. 19Ndipo Yoswa anati kwa Akani, Mwana wanga, ucitiretu ulemu Yehova Mulungu wa Israyeli, numlemekeze iye; nundiuze tsopano, wacitanji? usandibisire. 20Ndipo Akani anayankha Yoswa nati, Zoonadi, ndacimwira Yehova Mulungu wa Israyeli, ndacita zakuti zakuti; 21pamene ndinaona pazofunkha maraya abwino a ku Babulo, ndi masekeli mazana awiri a siliva, ndi cikute cagolidi, kulemera kwace masekeli makumi asanu, ndinazikhumbira ndi kuzitenga; ndipo taonani, ndazibisa m'nthaka pakati pa hema wanga, ndi siliva pansi pacepo. 22Pamenepo Yoswa anatuma mithenga, iwo nathamangira kuhema; ndipo taonani, zidabisika m'hema mwace ndi siliva pansi pace. 23Ndipo anazicotsa pakati pa hema, nabwera nazo kwa Yoswa ndi kwa ana onse a Israyeli, nazitula pamaso pa Yehova. 24Ndipo Yoswa, ndi Aisrayeli onse naye, anatenga Akani mwana wa Zera, ndi siliva, ndi marayawo, ndi cikute cagolidi, ndi ana ace amuna ndi akazi, ndi ng'ombe zace, ndi aburu ace, ndi nkhosa zace, ndi hema wace ndi zace zonse; nakwera nazo ku cigwa ca Akori. 25Ndipo Yoswa anati, Watisautsiranji? Yehova adzakusautsa lero lino. Ndipo, Aisrayeli onse anamponya miyala, nawatentha ndi moto, nawaponya miyala. 26Ndipo anamuuniikira mulu waukuru wamiyala, wokhalako kufikira lero lino; ndipo Yehova anatembenuka kusiya mkwiyo wace waukuru. Cifukwa cace anacha dzina lace la malowo, Cigwa ca Akori, mpaka lero lino.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Kupasulidwa kwa Ai

1Pamenepo Yehova anati kwa Yoswa, Usaope, kapena kutenga
nkhawa, tenga anthu onse a nkhondo apite nawe, ndipo tauka,
kwera ku Ai; taona, ndapereka m'dzanja lako mfumu ya ku Ai, ndi
anthu ace ndi mudzi wace ndi dziko lace; 2ndipo uzimcitira Ai ndi
mfumu yace monga umo unamcitira Yeriko ndi mfumu yace; koma
zofunkha zace ndi ng'ombe zace mudzifunkhire nokha; udziikire
anthu aja lire kukhonde kwa mudzi. 3Pamenepo anauka Yoswa, ndi
anthu onse a nkhondo, kuti akwere ku Ai; ndipo Yoswa anasankha
amuna zikwi makumi atatu, ndiwo ngwazi, nawatumiza apite
usiku, 4nawalamulira ndi kuti, Taonani, muzikhala olalira kukhonde
kwa mudzi; musakhalira kutali ndi mudzi, koma mukhale
okonzekeratu nonse; 5ndipo ine, ndi anthu onse ali nane,
tidzayandikira mudzi; ndipo kudzali, pamene aturuka kudzakomana
nafe, monga poyamba paja, tidzathawa pamaso pao; 6ndipo
adzaturuka kutitsata mpaka tidawakokera asiyane ndi mudzi;
pakuti adzanena, Atithawa pamaso pathu monga poyamba pala;
nafenso tidzathawa pamaso pao; 7pamenepo muziuka m'molalira
ndi kulowa m'mudzi; pakuti Yehova Mulungu wanu adzaupereka
m'manja mwanu. 8Ndipo kudzali, mutagwira mudzi, muzitentha
mudziwo ndi moto; muzicita monga mwa mau a Yehova; taonani,
ndakulamulirani. 9Ndipo Yoswa anawatuma, namuka iwo kulowa
m'molalira, nakhala pakati pa Beteli ndi Ai, kumadzulo kwa Ai;
koma Yoswa anakhala mwa anthu usiku uja.
10Ndipo Yoswa analawira mamawa, nayesa anthu, nakwera, iye ndi
akuru a Israyeli, pamaso pa anthu a ku Ai. 11Ndi anthu onse a
nkhondo okhala naye anakwera, nayandikira nafika pamaso pa
mudzi, namanga misasa kumpoto kwa Ai; koma pakati pa iye ndi
Ai panali cigwa. 12Ndipo anatenga amuna ngati zikwi zisanu,
nawaika m'molalira pakati pa Beteli ndi Ai, kumadzulo kwa
mudzi. 13Momwemo anaika anthu, khamu lonse lokhala kumpoto
kwa mudzi, ndi olalira ao kumadzulo kwa mudzi, ndipo usiku uja
Yoswa analowa pakati pa cigwa, 14Ndipo kunali, pamene mfumu ya
ku Ai anaciona, anafulumira iwo, nalawira mamawa, naturuka
amuna a m'mudzi kuthirana ndi Israyeli, iye ndi anthu ace onse,
poikidwiratu patsogolo pa cidikha; popeza sanadziwa kuti amlalira
kukhonde kwa mudzi. 15Ndipo Yoswa ndi Aisrayeli onse anaoneka
ngati a ku Ai alikuwathyola, nathawira njira ya
kucipululu. 16Pamenepo anthu onse okhala m'mudzi, anaitanidwa
awapitikitse, nampitikitsa Yoswa, nakokedwa kusiyana ndi
mudzi. 17Ndipo sanatsala mwamuna mmodzi yense m'Ai kapena
m'Beteli osaturukira kwa Israyeli; nasiya mudzi wapululu,
napitikitsa Israyeli. 18Pamenepo Yehova anati kwa Yoswa,

Tambasula nthungo iri m'dzanja lako iloze ku Ai, pakuti
ndidzaupereka m'dzanja lako. Ndipo Yoswa anatambasula
nthungoyo inali m'dzanja lace kuloza mudzi. 19Nauka msanga
olalirawo m'mbuto mwao, nathamanga pamene anatambasula
dzanja lace, nalowa m'mudzi, naugwira; nafulumira nayatsa
mudziwo. 20Pamene amuna a ku Ai anaceuka, anapenya, ndipo
taonani, utsi wa mudzi unakwera kumwamba; nasowa mphamvu
iwo kuthawa cakuno kapena cauko; ndi anthu othawira kucipululu
anatembenukira owapitikitsa. 21Ndipo pakupenya Yoswa ndi
Israyeli yense kuti olalirawo adagwira mudzi, ndi kuti utsi wa mudzi
unakwera, anabwerera, nawapha amuna a ku Ai. 22A kumudzinso
anawaturukira; potero anakhala pakati pa Israyeli, ena mbali yina,
ena mbali yina; ndipo anawakantha, mpaka sanatsala kapena
kupulumuka wa iwo ndi mmodzi yense. 23Koma mfumu ya ku Ai
anamgwira wamoyo, nadza naye kwa Yoswa. 24Ndipo kunali,
atatha Israyeli kupha nzika zonse za ku Ai, kuthengo, kucipululu
kumene anawapitikitsira, natha onse kugwa ndi lupanga lakuthwa
mpaka adathedwa onse, Aisrayeli onse anabwerera ku Ai,
naukantha ndi lupanga lakuthwa. 25Ndipo onse amene adagwa
tsiku lija, amuna ndi akazi, ndiwo zikwi khumi ndi ziwiri, anthu onse
a ku Ai. 26Popeza Yoswa sanabweza dzanja lace limene
anatambasula nalo nthungo, mpaka ataononga konse nzika zonse
za ku Ai. 27Koma ng'ombe ndi zofunkha za mudzi uwu Israyeli
anadzifunkhira monga mwa mau a Yehova amene analamulira
Yoswa. 28Ndipo Yoswa anatentha Ai, nausandutsa muunda ku
nthawi yonse, bwinja kufikira lero lino. 29Ndipo mfumu ya ku Ai,
anampacika pamtengo mpaka madzulo; koma polowa dzuwa
Yoswa analamulira kuti atsitse mtembo wace pamtengo; ndipo
anauponya polowera pa cipata ca mudzi; nauniikako mulu waukuru
wamiyala, mpaka lero lino.

Apereka nsembe nawerenga Malamulo a Mose ku Ebala ndi Gerizimu

30Pomwepo Yoswa anamangira Yehova Mulungu wa Israyeli guwa la
nsembe m'phiri la Ebala, 31monga Mose mtumiki wa Mulungu
adalamulira ana a Israyeli, monga mulembedwa m'buku la
cilamulo ca Mose, guwa la nsembe la miyala yosasema, yoti palibe
munthu anakwezapo citsulo; ndipo anafukizirapo Yehova nsembe
zopsereza, naphera nsembe zoyamika. 32Ndipo analembapo pa
miyalayi citsanzo ca cilamulo ca Mose, cimene analembera
pamaso pa ana a Israyeli. 33Ndipo Aisrayeli onse, ndi akuru ao, ndi
akapitao ao, ndi oweruza ao anaima cakuno ndi cauko ca likasa,
pamaso pa ansembe Alevi, akusenza likasa la cipangano la Yehova,
mbadwa ndi alendo omwe; ena a iwo pandunji pa phiri la Gerizimu,
ndi ena pandunji pa phiri la Ebala; monga Mose, mtumiki wa

Yehova, adalamulira poyamba pala kuti adalitse anthu a Israyeli, 34Atatero, anawerenga mau onse a cilamulo, dalitso ndi temberero, monga mwa zonse zolembedwa m'buku la cilamulo. 35Panalibe mau amodzi a zonse adazilamulira Mose osawerenga Yoswa pamaso pa msonkhano wonse wa Israyeli, ndi akazi ndi ang'ono, ndi alendo akuyenda pakati pao.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Yoswa 9

1Yoswa anyengedwa ndi Agibeoni napangana nao. Ndipo kunali,
pakumva ici mafumu onse a tsidya ilo la Yordano, kumapiri ndi
kucidikha, ndi ku madoko onse a nyanja yaikuru, pandunji pa
Lebano: Ahiti ndi Aamori, Akanani, Aperizi, Ahivi, ndi
Ayebusi; 2anasonkhana kuponyana ndi Yoswa ndi Israyeli, ndi mtima
umodzi.
3Koma pamene nzika za Gibeoni zinamva zimene Yoswa adacitira
Yeriko ndi Ai, 4zinacita momcenierera, nizimuka nizioneka ngati
mithenga, nizitenga matumba akale pa aburu ao, ndi matumba a
vinyo akale ndi ong'ambika ndi omangamanga; 5ndi nsapato
zakale za zigamba pa mapazi ao, nizibvala nsanza; ndi mikate
yonse ya kamba wao inali youma ndi yoyanga nkhungu. 6Ndipo
zinamuka kwa Yoswa kumisasa ku Giligala, niziti kwa iye ndi kwa
amuna a Israyeli, Tacokera dziko lakutali, cifukwa cace mupangane
nafe. 7Ndipo amuna a Israyeli anati kwa Ahivi, Kapena
mulimkukhala pakati pa ife, ndipo tipanganenji ndi inu? 8Koma
anati kwa Yoswa, Ndife akapolo anu. Pamenepo Yoswa anati kwa
iwo, Ndinu ayani? ndipo mufuma kuti 9Ndipo anati kwa iye,
Akapolo anu afumira dziko la kutalitali, cifukwa lea dzina la Yehova
Mulungu wanu; pakuti tidamva mbiri yace, ndi zonse anacita
m'Aigupto, 10ndi zonse anacitira mafumu awiri a Aamori okhala
tsidya lija la Yordano, Sihoni mfumu ya ku Hesiboni, ndi Ogi mfumu
ya ku Basana wokhala ku Asitorotu. 11Ndipo akuru athu ndi nzika
zonse za m'dziko mwathu zidanena nafe ndi kuti, Mutenge
m'dzanja lanu kamba wa paulendo, kakomane naoni, nimunene
nao, Ndife akapolo anu; ndipo tsopano mupangane nafe. 12Mkate
wathu uwu tinadzitengera kamba m'nyumba zathu, ukali wamoto,
tsiku loturuka Ife kudza kwanu kuno; koma tsopano, taonani, uli
wouma ndi woyaoga nkhungu; 13ndi matumba a vinyo awa
tinawadzaza akali atsopano; ndipo taonani, ang'ambika; ndi
malaya athu awa ndi nsapato zathu zatha, cifukwa ca ulendo
wocokera kutali ndithu. 14Pamenepo amunawo analandirako
kamba wao, osafunsira pakamwa pa Yehova. 15Ndipo Yoswa
anacitirana nao mtendere, napangana nao, akhale amoyo; ndi
akalonga a msonkhano anawalumbirira, 16Ndipo kunali, atatha
kupangana nao masiku atatu, anamva kuti ndiwo anansi ao, ndi
kuti kwao ndi pakati pao, 17Ndipo ana a Israyeli anayenda ulendo,
nafika ku midzi yap tsiku lacitatu. Koma midzi yao ndiyo Gibeoni,
ndi Cefira, ndi Beerotu ndi KiriyatuYearimu. 18Ndipo ana a Israyeli
sanawakantha, pakuti akalonga a msonkhano adawalumbirira kwa
Yehova, Mulungu wa Israyeli. Ndipo msonkhano wonse
unadandaula pa akalonga, 19Koma akalonga onse ananena kwa
msonkhano wonse, Tinawalumbirira kwa Yehova Mulungu wa

Israyeli, m'mwemo sitikhoza kuwacitira kanthu. 20Tidzawacitira ici, ndi kuwasunga amoyo; ungatigwere mkwiyo cifukwa ca lumbirolo tidawalumbirira. 21Ndipo akalonga ananena nao, Akhale ndi moyo; ndipo anasanduka akutema nkhuni, ndi otungira madzi msonkhano wonse; monga akalonga adanena nao. 22Ndipo Yoswa anawaitana, nanena nao, kuti, Mwatinyenga cifukwa ninji, ndi kuti, Tikhala kutaritari ndi inu, pokhala kwanu kuli pakati pa ife? 23Ndipo tsopano mukhale otembereredwa, palibe mmodzi wa inu adzamasuka wosakhala kapolo, ndi kutemera nkhuni, ndi kutungira madzi nyumba ya Mulungu wanga. 24Ndipo anamyankha Yoswa nati, Popeza anatiuzitsa akapolo anu kuti Yehova Mulungu wanu analamulira mtumiki wace Mose kukupatsani dziko lonseli, ndi kupasula nzika zonse za m'dziko pamaso panu; potero tinaopera kwambiri moyo wathu pamaso panu, ndipo tinacita cinthuci. 25Ndipo tsopano, taonani, tiri m'dzanja lanu; monga muyesa cokoma ndi coyenera kuticitira ife, citani. 26Pamenepo anawacitira cotero, nawalanditsa m'dzanja la ana a Israyeli, angawaphe. 27Ndipo tsiku lija Yoswa anawasandutsa akutema nkhuni, ndi otungira madzi msonkhanowo, ndi guwa la nsembe la Yehova, mpaka lero lino, pamalopo akadzasankha.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Cinkhondo ku Gibeoni

1Ndipo kunali, pamene Adoni-Zedeki mfumu ya Yerusalemu
anamva kuti Yoswa adalanda Ai, ndi kumuononga konse; nacitira Ai
ndi mfumu yace monga adacitira Yeriko ndi mfumu yace; ndi kuti
nzika za Gibeoni zinacitirana mtendere ndi Israyeli, nizikhala pakati
pao; 2anaopa kwambiri, popeza Gibeoni ndi mudzi waukuru,
monga wina wa midzi yacifumu, popezanso unaposa Ai kukula
kwace, ndi amuna ace onse ndiwo amphamvu. 3Cifukwa cace
Adoni-Zedeki anatuma kwa Hohamu, mfumu ya Hebroni, ndi kwa
Piraniu mfumu ya Yarimutu, ndi kwa Yafiya mfumu ya Lakisi, ndi
kwa Dibri mfumu va Egiloni, ndi kuti, 4Kwerani kwanga kuno, ndi
kundithandiza kuti tikanthe Gibeoni, pakuti unacitirana mtendere
ndi Yoswa ndi ana a Israyeli. 5Pamenepo mafumu asanu a Aamori,
ndiwo mfumu ya ku Yerusalemu, mfumu ya ku Hebroni, mfumu ya
ku Yarimutu, mfumu ya ku Lakisi, mfumu ya ku Egiloni
anasonkhana, nakwera iwo ndi makamu ao onse namanga misasa
pa Gibeoni, nauthira nkhondo. 6Ndipo amuna a ku Gibeoni
anatumira Yoswa mau kucigono ku Giligala, ndi kuti, Musalekerere
akapolo anu; mutikwerere msanga, ndi kutipulumutsa, ndi
kutithandiza; pakuti mafumu onse a Aamori, akukhala kumapiri
atisonkhanira. 7Pamenepo Yoswa anakwera kucokera ku Giligala,
iye ndi anthu onse a nkhondo pamodzi naye, ndi ngwazi
yose. 8Ndipo Yehova ananena ndi Yoswa, Usawaope, pakuti
ndawapereka m'dzanja lako; palibe mmodzi wa iwo adzaima
pamaso pako. 9Ndipo Yoswa anawadzidzimukitsa; popeza
anakwera kucokera ku Giligala usiku wonse. 10Ndipo Yehova
anawamwaza pamaso pa Israyeli, ndipo anawakantha
makanthidwe akuru ku Gibeoni, nawapitikitsa pa njira yokwera ya
Betihoroni, nawakantha mpaka Azeka, ndi mpaka Makeda. 11Ndipo
kunali, pakuthawa iwo pamaso pa Israyeli, potsikira pa Betihoroni,
Yehova anawagwetsera miyala yaikuru yocokera kumwamba
mpaka pa Azeka, nafa iwo; akufa ndi miyala yamatalala anacuruka
ndi iwo amene ana a Israyeli anawapha ndi lupanga.

Kuimitsidwa kwa dzuwa ndi mwezi

12Pomwepo Yoswa ananena kwa Yehova tsiku limene Yehova
anapereka Aamori pamaso pa ana a Israyeli; ndipo anati pamaso
pa Israyeli,

Dzuwa iwe, linda, pa Gibeoni,
Ndi Mwezi iwe, m'cigwa ca Aialo.

13Ndipo dzuwa linalinda, ndi mwezi unaima
Mpaka anthu adabwezera cilango adani ao.

Kodi ici sicilembedwa m'buku la Yasari? Ndipo dzuwa linakhala
pakati pa thambo, losafulumira kulowa ngati tsiku

lamphumphu. 14Ndipo panalibe tsiku lotere kale lonse kapena
m'tsogolomo, lakuti Yehova anamvera mau a munthu; pakuti
Yehova anathirira Israyeli nkhondo.
15Pamenepo Yoswa anabwerera, ndi Aisrayeli onse pamodzi naye,
ku cigono ca ku Giligala.
16Ndipo mafumu awa asanu anathawa, nabisala m'phanga la ku
Makeda, 17Ndipo anauza Yoswa ndi kuti, Mafumu asanuwa apezeka
obisala m'phanga la ku Makeda. 18Ndipo Yoswa anati,
Kunkhunizirani miyala yaikuru kukamwa kwa phanga, ndi kuikapo
anthu, awasunge; 19koma inu musaime, pitikitsani adani anu, ndi
kukantha a m'mbuyo mwao; musawalole alowe m'midzi mwao;
pakuti Yehova Mulungu wanu anawapereka m'dzanja lanu. 20Ndipo
kunali, Yoswa ndi ana a Israyeli atatha kuwakantha, makanthidwe
akurukuru mpaka atatha psiti, ndipo otsala a iwo atalowa m'midzi
ya malinga, 21anthu onse anabwerera kucigono kwa Yoswa pa
Makeda ndi mtendere. Palibe munthu anacitira cipongwe mmodzi
yense wa ana a Israyeli. 22Pamenepo Yoswa anati, Tsegula
pakamwa pa phanga ndi kunditurutsira m'phanga mafumu
asanuwo. 23Ndipo anatero, naturutsira m'phanga mafumu
asanuwo, mfumu ya ku Yerusalemu, mfumu ya ku Hebroni, mfumu
ya ku Yarimutu, mfumu ya ku Lakisi, mfumu ya ku Egiloni. 24Ndipo
kunali, ataturutsira Yoswa mafumu awa, Yoswa anaitana amuna
onse a Israyeli, ndipo anati kwa akazembe a anthu a nkhondo
amene anamuka naye, Yandikirani, pondani pa makosi a mafumu
awa. Nayandikira iwo, naponda pa makosi ao. 25Pamenepo Yoswa
ananena nao, Musaope, musatenge nkhawa; khalani amphamvu,
nimulimbike mtima; pakuti Yehova adzatero ndi adani: anu onse
amene mugwirana nao: nkhondo. 26Ndipo atatero, Yoswa
anawakantha nawapha, nawapacika pa mitengo isanu;
nalikupacikidwa pa mitengo mpaka madzulo. 27Ndipo kunali,
nthawi yakulowa dzuwa, Yoswa analamulira kuti awatsitse
kumitengo; ndipo anawataya m'phanga m'mene adabisala; naika
miyala yaikuru pakamwa pa phanga, mpaka lero lomwe lino.

Midzi ya kumwera igonja kwa Yoswa

28Ndipo Yoswa anagwira Makeda tsiku lomwe lija ndi kuukantha ndi
lupanga lakuthwa, ndi mfumu yace yom we; anawaononga konse,
ndi amoyo onse anali m'mwemo, osasiyapo ndi mmodzi yense,
nacitira mfumu ya ku Makeda monga anacitira mfumu ya ku Yeriko.
29Pamenepo Yoswa ndi Aisrayeli onse naye anapitirira kucokera ku
Makeda kumka ku Libina, nathira nkhondo pa Libina; 30ndipo
Yehova anapereka uwunso, ndi mfumu yace m'dzanja la Israyeli;
ndipo anaukantha ndi lupanga lakuthwa, ndi amoyo onse anali
m'mwemo, osasiyamo ndi mmodzi yense; namcitira mfumu yace
monga anacitira mfumu ya ku Yeriko.

31Ndipo Yoswa, ndi Aisrayeli onse naye, anapitirira kucokera ku
Libina kumka ku Lakisi; namanga misasa, nathira nkhondo pa
uwo; 32napereka Yehova Lakisi m'dzanja la Israyeli, ndipo
anaulanda tsiku laciwiri, naukantha ndi lupanga lakuthwa, ndi
amoyo onse anali m'mwemo monga mwa zonse anacitira Libina.
33Pamenepo Horamu mfumu ya Gezere anakwera kudzathandiza
Lakisi; ndipo Yoswa anamkantha iye ndi anthu ace mpaka
sanamsiyira ndi mmodzi yense.
34Ndipo Yoswa, ndi Aisrayeli onse naye, anapitirira kucokera ku
Lakisi mpaka ku Egiloni; namanga nrisasa, nathira
nkhondo. 35Naulanda tsiku lomwelo, naukantha ndi lupanga
lakuthwa, nawaononga konse amoyo onse anali m'mwemo tsiku
lomwelo, monga mwa zonse anacitira Lakisi.
36Ndipo Yoswa ndi Aisrayeli onse naye anakwera kucokera ku
Egiloni mpaka ku Hebroni, nauthira nkhondo; 37naulanda,
naukantha ndi lupanga lakuthwa, ndi mfumu yace ndi midzi yace
yonse, ndi amoyo onse anali m'mwemo, osasiyapo ndi mmodzi
yense, monga mwa zonse anacitira Egiloni; koma anauononga
konse, ndi amoyo onse anali m'mwemo.
38Pamenepo Yoswa, ndi Aisrayeli onse naye, anabwerera kudza ku
Dibiri, nauthira nkhondo, 39naulanda, ndi mfumu yace ndi midzi
yace yonse; naikantha ndi lupanga lakuthwa, naononga konse
amoyo onse anali m'mwemo; sanasiya ndi mmodzi yense; monga
anacitira Hebroni momwemo anacitira Dibiri ndi mfumu yace,
monganso anacitira Libina ndi mfumu yace.
40Motero Yoswa anakantha dziko lonse, la kumapiri, la kumwela, la
kucidikha, la kuzigwa, ndi mafumu ao onse; sanasiyapo ndi
mmodzi yense; koma anaononga psiti zonse zampweya, monga
Yehova Mulungu wa Israyeli adalamulira. 41Ndipo Yoswa
anawakantha kuyambira Kadesi-Barinea mpaka ku Gaza, ndi dziko
lonse la Goseni mpaka ku Gibeoni. 42Ndipo Yoswa anagwira
mafwnu awa onse ndi dziko lao nthawi yomweyi; cifukwa Yehova
Mulungu wa Israyeli anathirira Israyeli nkhondo. 43Pamenepo
Yoswa ndi Aisrayeli onse naye, anabwerera kucigono ku Giligala.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Yoswa agonjetsa mafumu a kumpoto

1Ndipo kunali, pamene Yabini mfumu ya ku Hazoro anacimva,
anatwna kwa Yabobu mfumu ya ku Madoni, ndi kwa mfumu ya ku
Simironi, ndi kwa mfumu ya ku Akasafu, 2ndi kwa mafwnu
akukhala kumpoto kumapiri, ndi kucigwa kwumwela kwa Kineroto,
ndi kucidikha, ndi ku mitunda ya Doro kwnadzulo; 3kwa Akanani
kwn'mawa ndi kumadzulo, ndi kwa Aamori ndi Ahiti, ndi Aperizi ndi
Ayebusi kumapiri, ndi kwa Ahivi kunsi kwa Herimoni, m'dziko la
Mizipa. 4Ndipo anaturuka, iwo ndi makamu ao onse nao, anthu
ambiri, kucuruka kwao ngati mcenga uli m'mphepete mwa nyanja;
ndi akavalo ndi magareta ambirimbiri. 5Ndipo mafwnu awa onse
anasonkhana, nadza namanga pamodzi ku madzi a Meromu,
kumthira Israyeli nkhondo. 6Koma Yehova anati kwa Yoswa, Usaope
cifukwa ca iwowa; pakuti mawa, dzuwa lino ndidzawapereka onse
ophedwa pamaso pa Israyeli; uziwadula mitsindo akavalo ao, ndi
kutentha agareta ao ndi moto. 7Ndipo Yoswa, ndi anthu onse a
nkhondo naye, anawadzera modzidzimutsa ku madzi a Meromu,
nawagwera. 8Ndipo Yehova anawapereka m'dzanja la Israyeli,
ndipo anawakantha, nawapitikitsa mpaka ku Zidoni waukulu, ndi
ku MiseripotuMaimu, ndi ku cigwa ca Mizepe kum'mawa;
nawakantha mpaka sanawasiyira ndi mmodzi yense. 9Ndipo Yoswa
anawacitira monga Yehova adamuuza: nadula akavalo ao mitsindo,
natentha magareta ao ndi moto.
10Ndipo Yoswa anabwerera m'mbuyo nthawi imeneyi nalanda
Hazori nakantha mfumu yace ndi lupanga; pakuti kale Hazori unali
waukuru wa maufumu aja onse. 11Ndipo anakantha amoyo onse
anali m'mwemo, ndi lupanga lakuthwa, ndi kuwaononga konse,
osasiyapo ndi mmodzi yense wakupuma mpweya; ndipo anatentha
Hazori ndi moto. 12Ndipo Yoswa analanda midzi yonse ya mafumu
awa, ndi mafumu ao omwe nawakantha ndi lupanga lakuthwa,
nawaononga konse; monga Mose mtumiki wa Yehova
adalamulira. 13Koma midzi yonse yomangidwa pa zitunda zao
Israyeli sanaitentha, koma wa Hazori wokha; wnenewu Yoswa
anautentha. 14Ndi zofunkha zonse za midzi iyi ndi ng'ombe ana a
Israyeli anadzifunkhira; koma anakantha ndi lupanga lakuthwa
anthu onse mpaka adawaononga osasiyapo ndi mmodzi yense
wopuma mpweya. 15Monga Yehova adalamulira Mose mtumiki
wace, momwemo Mose analamulira Yoswa; momwemonso anacita
Yoswa; sanacotsapo mau amodzi pa zonse Yehova adalamulira
Mose.
16Motero Yoswa analanda dziko lonselo, la kumapiri, ndi la
kumwera, ndi dziko lonse la Goseni, ndi dziko la kucidikha, ndi la
kucigwa; ndi la kwnapiri la Israyeli, ndi la ku cidikha

cace; 17kuyambira phiri la Halaki lokwera kumka ku Seiri, mpaka
Baala-gadi m'cigwa ca Lebano patsinde pa phiri la Herimoni;
nagwira mafwnu ao onse, nawakantha, nawapha. 18Yoswa anathira
nkhondo mafwnu awa onse nthawi yaikuru. 19Palibe mudzi
wakupangana mtendere ndi ana a Israyeli, koma Ahivi okhala
m'Gibeoni; anaigwira yonse ndi nkhondo. 20Pakuti cidadzera kwa
Yehova kulimbitsa mitima yao kuti athirane nao Aisrayeli nkhondo
kuti iye awaononge konse, kuti asawacitire cifundo koma
awaononge, monga Yehova adalamulira Mose.
21Ndipo Yoswa anadza nthawi yomweyo, napasula Aanaki
kuwacotsa kumapiri, ku Hebroni, ku Dibiri, ku Anabi, ndi ku mapiri
onse a Yuda, ndi ku mapiri onse a Israyeli; Yoswa anawaononga
konse, ndi midzi yao yomwe. 22Panalibe Aanaki otsala m'dziko la
ana a Israyeli; koma m'Gaza, ndi m'Gati ndi m'Asidodo anatsalamo
ena. 23Motero Yoswa analanda dziko lonse monga mwa zonse
Yehova adazinena kwa Mose; ndipo Yoswa analipereka kwa Israyeli,
likhale lao lao, pfuko liri lonse gawo lace. Ndipo dziko linapumula
nkhondo.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Mafumu amene ana a Israyeli anawakantha

1Ndipo awa ndi mafumu a dzikolo amene ana a Israyeli
anwakantha, nalanda dziko lao tsidya la Yordano kum'mawa,
kuyambira cigwa ca Arimoni, mpaka phiri la Herimoni, ndi cidikha
conse ca kum'mawa; 2Sihoni mfumu ya Aaroori wokhala
m'Hesiboni, wocita ufumu kuyambira ku Aroeri ndiwo m'mphepete
mwa cigwa ca Arinoni, ndi pakati pa cigwa ndi pa Gileadi wogawika
pakati, kufikira mtsinje wa Yaboki, ndiwo malire a ana a
Amoni; 3ndi pacidikha mpaka nyanja ya Kineroti kum'mawa, ndi
mpaka nyanja ya kucidikha, ndiyo Nyanja ya Mcere kum'mawa,
njira ya Beti-Yesimoti; ndi kumwela pansi pa matsikiro a
Pisiga. 4Nalandanso malire a Ogi mfumu ya Basana wotsala wa
Arefai, wokhala ku Asitarotu ndi ku Edrei, 5nacita ufumu m'phiri la
Herimoni, ndi m'Saleka, ndi m'Basana lonse, mpaka malire a
Agesuri, ndi a Maakati, ndi Gileadi wogawika pakati, malire a
Sihoni mfumu ya ku Hesiboni. 6Mose mtumiki wa Yehova ndi ana a
Israyeli anawakantha; ndi Mose mtumiki wa Yehova analipereka
kwa Arubeni, ndi Agadi ndi pfuko la Manase logawika pakati,
likhale colowacao.
7Ndipo awa ndi mafumu a dzikolo amene Yoswa ndi ana a Israyeli
anawakantha tsidya lija la Yordano kumadzulo, kuyambira Baala-
gadi m'cigwa ca Lebano mpaka phiri la Halaki lokwera kumka ku
Seiri; ndipo Yoswa analipereka kwa mapfuko a Israyeli, likhale lao
lao, monga mwa magawo ao; 8kumapiri ndi kucigwa, ndi kucidikha,
ndi kumatsikiro, ndi kucipululu, ndi kumwela: Ahiti, Aamori, ndi
Akanani, Aperizi, Ahivi ndi Ayebusi: 9mfumu ya ku Yeriko, imodzi;
mfumu ya ku Ai, ndiwo m'mbali mwa Beteli, imodzi; 10mfumu ya ku
Yerusalemu, imodzi; mfumu ya ku Hebroni, imodzi; mfumu ya ku
Yarimutu, imodzi; 11mfumu ya ku Lakisi, imodzi; 12mfumu ya ku
Egiloni, imodzi; mfumu ya ku Gezere, imodzi; 13mfumu ya ku Dibiri,
imodzi; mfumu ya ku Gederi, imodzi; 14mfumu ya ku Horima,
imodzi; mfumu ya ku Haradi, imodzi; 15mfumu ya ku Libina,
imodzi; mfumu ya ku Adulamu, imodzi; 16mfumu ya ku Makeda,
imodzi; mfumu ya ku Beteli, imodzi; 17mfumu ya ku Tapuwa,
imodzi; mfumu ya ku Heferi, imodzi; 18mfumu ya ku Afeki, imodzi;
mfumu ya ku Lasaroni, imodzi; 19mfumu ya ku Madoni, imodzi;
mfumu ya ku Hazori, imodzi; 20mfumu ya ku Simironi-meroni,
imodzi; mfumu ya ku Akasafu, imodzi; 21mfumu ya ku Taanaki,
imodzi; mfumu ya ku Megido, imodzi; 22mfumu ya ku Kadesi,
imodzi; mfumu ya ku Yokineamu ku Karimeli, imodzi; 23mfumuya
ku Doro, mpaka ponyamuka pa Doro, imodzi; mfumu ya ku Goimu
m'Giligala, imodzi; 24mfumu ya ku Tiriza, imodzi. Mafumu awa onse
ndiwo makumi atatu ndi imodzi.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Cigawo ca dziko la kum'mawa kwa Yordano

1Ndipo Yoswa anakalamba, wa zaka zambiri; ndipo Yehova
ananena naye, Wakalamba, wa zaka zambiri, ndipo latsala dziko
lalikurukuru, alilandire colowa cao, 2Dziko lotsala ndilo: malire onse
a Afilisti, ndi Agesuri onse, 3kuyambira Sihoro wokhala cakuno ca
Aigupto mpaka malire a Ekironu kumpoto, loyesedwa la Akanani;
akalonga asanu a Afilisti, a ku Gaza, ndi a ku Asidodi, a ku Asekelo,
a ku Giti, ndi a ku Ekiro, ndi Ahivi; 4kumwela dziko lonse la
Akanani, ndi Meara ndiwo wa Asidoni, mpaka ku Afeka, mpaka ku
malire a Aaroori; 5ndi dziko la Agebili, ndi Lebano lonse kum'mawa,
kuyambira Baala-gadi pa tsinde la phiri la Herimoni, mpaka
polowera pace pa Hamati; 6nzika zonse za kumapiri kuyambira
Lebano, mpaka Misirepotumaimu, Asidoni onse; ndidzawainga
pamaso pa ana a Israyeli, koma limeneli uwagawire Aisrayeli,
likhale colowa cao, monga ndinakulamulira. 7Ndipo tsopano
uwagawire mapfuko asanu ndi anai, ndi pfuko la Manase logawika
pakati, dziko ili likhale colowa cao. 8Pamodzi ndi iye Arubeni ndi
Agadi analandira colowa cao, cimene Mose adawapatsa tsidya ilo
la Yordano kum'mawa, monga Mose mtumiki wa Yehova
anawapatsa; 9kuyambira pa Aroeri, wokhala m'mphepete mwa
cigwa ca Arinoni, ndi mudzi uti pakati pa cigwa, ndi cidikha conse
ca Medeba mpaka ku Diboni; 10ndi midzi yonse ya Sihoni mfumu
ya Aamori, wakucita ufumu m'Hesiboni, mpaka malire a ana a
Amoni; 11ndi Gileadi, ndi malire a Agesuri, ndi Amaakati, ndi phiri
lonse la Herimoni, ndi Basana ionse mpaka ku Saleka; 12ufumu
wonse wa Ogi m'Basana, wakucita ufumu m'Asitarotu, ndi m'Edrei
(yemweyo anatsala pa otsala a Arefai); pakuti Mose anakantha
awa, nawainga. 13Koma ana a Israyeli sanainga Agesuri kapena
Amaakati; koma Gesuri, ndi Maakati amakhala pakati pa Israyeli,
mpaka lero lino. 14Koma pfuko la Levi sanalipatsa colowa; nsembe
za Yehova Mulungu wa Israyeli, zocitika ndi moto, ndizo colowa
cace, monga iye adanena naye.
15Ndipo Mose anapatsira pfuko la ana a Rubeni monga mwa
mabanja ao. 16Malire ao anayambira ku Aroeri wokhala
m'mphepete mwa cigwa ca Arinoni, ndi mudzi uli pakati pa cigwa
ndi cidikha conse ca ku Medeba; 17Hesiboni ndi midzi yace yonse
yokhala pacidikha; Diboni, ndi Bamoto-baala ndi Betibaala-
Meoni; 18ndi Yahaza ndi Kedemotu, ndi Mefaata; 19ndi Kinyataimu,
ndi Sibima, ndi Zeretisahara, m'phiri la kucigwa; 20ndi Beti-peori,
ndi matsikiro a Pisiga, ndi Beti-yesimotu; 21ndi midzi yonse ya
kucidikha, ndi ufumu wonse wa Sihoni mfumu ya Aamori, wocita
ufumu m'Hesiboni, amene Mose anamkantha pamodzi ndi
akalonga a Midyani, Evi, ndi Rekemu, ndi Zuri, ndi Huri ndi Reba,

akalonga a Sihoni, nzika za m'dziko. 22Ana a Israyeli anaphanso ndi
lupanga Balamu mwana wa Beori, mlauli uja, pamodzi ndi ena
adawaphawo. 23Ndipo malire a ana a Rubeni ndiwo Yordano ndi
malire ace. Ndico colandira ca ana a Rubeni monga mwa mabanja
ao, midzi yace ndi miraga yace.
24Ndipo Mose anapatsira pfuko la Gadi, ana a Gadi, monga mwa
mabanja ao. 25Ndipo malire ao ndiwo Yazeri, ndi midzi yonse ya
Gileadi, ndi dziko la ana a Amoni logawika pakati, mpaka ku Aroeri,
wokhala cakuno ca Raba; 26ndi kuyambira Hesiboni mpaka Ramati-
Mizipe, ndi Betonimu; ndi kuyambira Mahanaimu mpaka malire a
Dibiri; 27ndipo m'cigwa Betiharamu, ndi Beti-nimra, ndi Sukoti, ndi
Zafoni, cotsala ca ufumu wa Sihoni mfumu ya Hesiboni, Yoidano
ndi malire ace, mpaka malekezero a nyanja ya Kinereti, tsidya lija
la Yordano kum'mawa. 28Ici ndi colowa ca ana a Gadi, monga mwa
mabanja ao, midzi yace ndi miraga yace.
29Mose anaperekanso colowa kwa pfuko la Manase logawika
pakati, ndico ca pfuko la Manase logawika pakati monga mwa
mabanja ao. 30Ndipo malire ao anayambira ku Mahanaimu, Basana
lonse, ufumu wonse wa Ogi mfumu ya ku Basana, ndi midzi yonse
ya Yairi, yokhala m'Basana, midzi makumi asanu ndi limodzi; 31ndi
Gileadi logawika pakati, ndi Asitarotu ndi Edrei, midzi ya ufumu wa
Ogi m'Basana, inali ya ana a Makiri mwana wa Manase, ndiwo ana
a Makiri ogawika pakati, monga mwa mabanja ao.
32Izi ndi zolowazi Mose anazigawira m'zidikha za Moabu, tsidya ilo
la Yordano ku Yeriko, kum'mawa. 33Koma pfuko la Levi, Mose
analibe kulipatsa colowa: Yehova Mulungu wa lsrayeli, ndiye
colowa cao, monga ananena nao.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Kalebe alandira Hebroni

1Ndipo awa ndi maiko ana a Israyeli anawalanda m'dziko la Kanani,
amene Eleazare wansembe, ndi Yoswa mwana wa Nuni, ndi akulu a
nyumba za atate a mapfuko a ana a Israyeli,
anawagawira. 2Kulandira kwao kunacitika ndi kulota maere, monga
Yehova adalamulira mwa dzanja la Mose, kunena za mapfuko
asanu ndi anai ndi pfuko logawika pakati. 3Pakuti Mose adapatsa
mapfuko awiri, ndi pfuko logawika pakati, colowa tsidya ito la
Yordano; koma sanapatsa Alevi colowa pakati pao, 4Pakuti ana a
Yosefe ndiwo mapfuko awiri, Manase ndi Efraimu; ndipo
sanawagawira Alevi kanthu m'dziko, koma midzi yokhalamo ndi
dziko lozungulirako likhale la zoweta zao ndi cuma cao. 5Monga
Yehova analamulira Mose, momwemo ana a Israyeli anacita,
nagawana dziko.
6Pamenepo ana a Yuda anadza kwa Yoswa ku Giligala; ndi Kalebe
mwana wa Yefune Mkenizi ananena naye, Mudziwa cimene Yehova
adanena kwa Mose munthu wa Mulungu za ine ndi za inu
m'KadesiBarinea. 7Ndinali ine wa zaka makumi anai muja Mose
mtumiki wa Yehova anandituma kucokera ku Kadesi-Barinea,
kukazonda dziko; ndipo ndinambwezera mau, monga momwe
anakhala mumtima mwanga. 8Koma abale anga amene anakwera
nane anasungunutsa mitima ya anthu; koma ine ndinamtsata
Yehova Mulungu wanga ndi mtima wanga wonse. 9Ndipo Mose
analumbira tsiku lomwelo ndi kuti, Zedi, dzikoli phazi lako
lapondapo lidzakhala colowa cako, ndi ca ana ako kosalekeza,
cifukwa unatsata Yehova Mulungu wanga ndi mtima
wonse. 10Ndipo tsopano, taonani, Yehova anandisunga ndi moyo,
monga ananena, zaka izi mak umi anai ndi zisanu kuyambira
nthawi ija Yehova ananena kwa Mose mau awa, poyenda Israyeli
m'cipululu; ndipo tsopano taonani, ndine wa zaka makumi asanu
ndi atatu, kudza zisanu lero lino. 11Koma lero lino ndiri
wamphamvu monga tsiku lija anandituma Mose; monga mphamvu
yanga pamene paja, momwemo mphamvu yanga tsopano, kugwira
nkhondo, ndi kuturuka ndi kulowa. 12Ndipo tsopano, ndipatseni
phiri ili limene Yehova ananenera tsiku lija; pakuti udamva tsiku
lijalo kuti Aanaki anali komweko, ndi midzi yaikuru ndi yamalinga;
kapena Yehova adzakhala ndi ine, kuti ndiwaingitse monga
ananena Yehova. 13Pamenepo Yoswa anamdalitsa, napatsa Kalebe
mwana wa Yefune Hebroni likhale colowa cace. 14Cifukwa cace
Hebroni likhala colowa cace ca Kalebe mwana wa Yefune Mkenizi
mpaka lero lino; popeza anatsata Yehova Mulungu wa Israyeli ndi
mtima wonse. 15Koma kale dzina la Hebroni linali mudzi wa Ariba,

ndiye munthu wamkuru pakati pa Aanaki. Ndipo dziko linapumula nkhondo.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Malire a Yuda

1Ndipo gawo la pfuko la ana a Yuda monga mwa mabanja ao
linafikira malire a Edomu, ku cipululu ca Zini kumwera, ku
malekezero a kumwera. 2Ndi malire ao a kumwera, anayambira ku
malekezero a Nyanja ya Mcere, ku nyondo yoloza
kumwera; 3naturuka kumwela kwa cikweza ca Akarabi, napitirira
ku Zini, nakwera kumwera kwa Kadesi-Barinea, napitirira ku
Hezironi, nakwera ku Adara, nazungulira ku Karika; 4napitirira ku
Azimoni, naturuka ku mtsinje wa Aigupto; ndi malekezero a
malirewa anali ku Nyanja Yaikuru; awa ndi malire anu a
kumwera. 5Ndi malire a kum'mawa ndiwo Nyanja ya Mcere, mpaka
mathiriro ace a Yordano. Ndi malire a kumpoto anayambira nyondo
ya nyanja ku mathiriro a Yordano; 6nakwera malire kumka ku Beti-
hogila, napitirira kumpoto kwa Beti-araba; nakwera malire kumka
ku mwala wa Bohani mwana wa Rubeni; 7nakwera malire kumka ku
Dibiri, kucokera ku cigwa ca Akori, ndi kumpoto kupenyera Giligala
ndiko kundunji kwa cikweza ca Adumi, ndiko kumwela kwa mtsinje;
napitirira malire kumka ku madzi a Enisemesi, ndi maturukiro ace
anali ku Eni-rogeli; 8nakwera malire kumka ku cigwa ca mwana wa
Hinomu, kumbali kwa Ayebusi, kumwela, ndiko Yerusalemu;
nakwera malire kumka kumwamba kwa phiri lokhala patsogolo pa
cigwa ca Hinomu kumadzulo, ndilo ku mathero ace a cigwa ca
Refai kumpoto, 9Ndipo analemba malire kuyambira pamwamba pa
phiri mpaka citsime ca madzi ca Nefitoa, naturukira malire ku
midzi ya phiri la Efroni; ndipo analemba malire kumka ku Baala,
ndiwo Kiriyati-Yearimu. 10Ndipo malire anazungulira kuyambira ku
Baala kumka kumadzulo, ku phiri la Seiri, napitirira kumbali kwa
phiri la Yearimu kumpoto, ndilo Kesaloni, natsikira ku Beti-semesi,
napitirira ku Timina; 11naturuka malire kumka ku mbali ya Ekroni
kumpoto; ndipo analemba malire kumka ku Sikeroni, napitirira ku
phiri la Baala, naturuka ku Yabindi; ndipo maturukiro a malire anali
kunyanja. 12Ndi malire a kumadzulo anali ku Nyanja Yaikuru ndiwo
malire ace. Awa ndi malire a ana a Yuda pozungulira monga mwa
mabanja ao.

13Koma Yoswa anampatsa Kalebe mwana wa Yefune gawo mwa
ana a Yuda, monga Yehova adamlamulira, ndiwo mudzi wa Ariba,
ndiye atate wa Anaki, ndiwo Hebroni. 14Ndipo Kalebe anaingitsako
ana amuna atatu a Anaki, ndiwo Sesai, ndi Ahimani, ndi Talimai,
ana a Anaki. 15Nakwera komweko kumka kwa nzika za Dibiri; koma
kale dzina la Dibiri ndilo Kiriyati-Seferi. 16Ndipo Kalebe anati, iye
amene akantha Kiriyati-Seferi, naulanda, yemweyo ndidzampatsa
Akisa mwana wanga akhale mkazi wace. 17Ndipo Otiniyeli mwana
wa Kenazi, mbale wace wa Kalebe, anaulanda; ndipo anampatsa

Akisa mwana wace akhale mkazi wace. 18Ndipo kunali, m'mene
anamdzera, anamkangamiza mwamuna wace kuti apemphe atate
wace ampatse munda; ndipo anatsika pa buru; pamenepo Kalebe
ananena naye, Ufunanji? 19Nati iye, Mundipatse dalitso; popeza
mwandipatsa dziko la kumwela, ndipatseninso zitsime za madzi.
Pamenepo anampatsa zitsime za kumtunda, ndi zitsime za kunsi.
20Ici ndi colowa ca pfuko la ana a Yuda monga mwa mabanja ao.
21Ndipo midzi ya ku malekezero a pfuko la ana a Yuda ku malire a
Edomu, kumwela ndiwo, Kabizeeli ndi Ederi, ndi Yaguri; 22ndi Kina
ndi Dimona, ndi Adada; 23ndi Kedesi, ndi Hazori, ndi Itinani; 24Zifi
ndi Telemu ndi Bealoti; 25ndi Hazorihadata, ndi Kerioti-hezirondi,
ndiwo Hazori; 26Amamu ndi Sema ndi Moloda; 27ndi Hazara-gada,
ndi Hesimoni, ndi Beti-peleti; 28ndi Hazara-suala, ndi Beereseba,
ndi Bizioti; 29Baala, ndi Iyimu, ndi Ezemu; 30ndi Elitoladi, ndi Kesili
ndi Horima; 31ndi Zikilaga, ndi Madimana ndi Sanasana; 32ndi
Lebaoti, ndi Siliimu, ndi Aini ndi Rimoni; midzi yonse ndiyo makumi
awiri kudza isanu ndi inai; pamodzi ndi miraga yao.
33Ku cigwa, Esitaoli, ndi Zora ndi Asina; 34ndi Zoona, ndi
Eniganimu, Tapua, ndi Enamu; 35Yarimutu, ndi Adulamu, Soko, ndi
Azeka; 36ndi Saaraimu, ndi Aditaimu, ndi Gedera, ndi Gederotaimu;
midzi khumi ndi inai pamodzi ndi miraga yao.
37Zenani, ndi Hadasa, ndi Migidala-gadi; 38ndi Dilani, ndi Mizipe,
ndi Yokiteeli; 39Lakisi ndi Bozikatu ndi Egiloni; 40ndi Kaboni, ndi
Lamasi, ndi, Kitilisi; 41ndi Gaderotu, Beti-dagoni, ndi Naama, ndi
Makeda; midzi khumi ndi isanu ndi umodzi pamodzi ndi miraga
yao.
42Libina ndi Eteri ndi Asana; 43ndi Ifita ndi Asina ndi Nezibi; 44ndi
Kehila ndi Akisibu, ndi Maresa; midzi isanu ndi inai pamodzi ndi
miraga yao.
45Ekroni pamodzi ndi midzi yace ndi miraga yao; 46kuyambira ku
Ekroni mpaka kunyanja, yonse ya ku mbali ya Asidodo, pamodzi
ndi miraga yao.
47Asidodo, midzi yace ndi miraga yace; Gaza, midzi yace ndi
miraga yace; mpaka mtsinje wa Aigupto, ndi nyanja yaikuru ndi
malire ace.
48Ndi kumapiri Samiri, ndi Yatiri, om Soko; 49ndi Dana, ndi
Kiriyatisana, ndiwo Dibiri; 50ndi Anabi, ndi Esitemo, ndi
Animu; 51ndi Goseni, ndi Holoni, ndi Gilo; midzi khumi ndi umodzi
pamodzi ndi miraga yao.
52Arabu, ndi Duma, ndi Esana; 53ndi Yanimu, ndi Beti-tapua, ndi
Apeka; 54ndi Humita, ndi Kiriyatiariba, ndiwo Hebroni, ndi Ziori;
midzi isanu ndi inai pamodzi ndi miraga yao.

55Maoni, Karimeli, ndi Zifu, ndi Yuta; 56ndi Yesireeli, ndi Yokideamu,
ndi Zoona; 57Kaini, Gibea ndi Timina; midzi khumi pamodzi ndi
miraga yao.
58Haluli, Beti-zuru, ndi Gedori, 59ndi Maaratu, ndi Bete-anotu, ndi
Elitekoni; midzi isanu ndi umodzi pamodzi ndi miraga yao.
60Kiriyata-Baala, ndiwo KiriyatiYearimu ndi Raba; midzi iwiri
pamodzi ndi miraga yao.
61M'cipululu, Beti-araba, Midini, ndi Sekaka; 62ndi Nibisani, ndi
Mudzi wa Mcere, ndi En-gedi; midzi isanu ndi umodzi pamodzi ndi
miraga yao.
63Koma ana a Yuda sanakhoza kuingitsa Ayebusi, nzika za
Yerusalemu: m'mwemo Ayebusi anakhala pamodzi ndi ana a Yuda,
ku Yerusalemu, mpaka lero lino.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Malire a Efraimu

1Ndipo gawo La ana a Yosefe linaturuka kucokera ku Yordano ku
Yeriko, ku madzi a Yeriko kum'mawa, kucipululu, nakwera kucokera
ku Yeriko kumka kumapiri ku Beteli; 2naturuka ku Beteli kumka ku
Luzi, napitirira kumka ku malire a Aariki, ku Atarotu; 3natsikira
kumadzulo kumka ku malire a Ayafeleti, ku malire a Beti-horoni wa
kunsi, ndi ku Gezeri; ndi maturukiro ace anali kunyanja. 4Motero
ana a Yosefe, Manase ndi Efraimu analandira colowa cao, 5Ndipo
malire a ana a Efraimu, monga mwa mabanja ao, ndiwo: malire a
colowa cao kum'mawa ndiwo Atarotu-Adara, mpaka Betihoroni wa
kumtunda; 6naturuka malire kumadzulo ku Mikametatu kumpoto;
nazungulira malire kum'mawa kumka ku Taanatu-silo, naupitirira
kum'mawa kwace kwa Yanoa: 7natsika kucokera ku Yanoa, kumka
ku Atarotu, ndi ku Naara, nafika ku Yeriko, naturuka ku
Yordano. 8Kuyambira ku Tapua malire anamuka kumadzulo ku
mtsinje wa Kana; ndi maturukiro ace anali kunyanja. Ici ndi colowa
ca pfuko la ana a Efraimu monga mwa mabanja ao; 9pamodzi ndi
midzi adaipatulira ana a Efraimu pakati pa colowa ca ana a
Manase, midzi yonse pamodzi ndi miraga yao. 10Ndipo a
sanaingitsa Akanani akukhala m'Gezeri; koma Akanani anakhala
pakati pa Efraimu, kufikira lero lino, nawasonkhera msonkho.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Malire a Manase

1Gawo la pfuko la Manase ndi ili: pakuti anali woyamba wa Yosefe.
Makiri mwana woyamba wa Manase, atate wa Gileadi, popeza
ndiye munthu wa nkhondo, anakhala nayo Gileadi ndi
Basana. 2Ndipo maere anagwera ana ena otsala a Manase monga
mwa mabanja ao; ana a Abiezere ndi ana a Heleki, ndi ana a
Asiriyeli, ndi ana a Sekemu ndi ana a Hefere, ndi ana a Semida;
awa ndi ana amuna a Manase mwana wa Yosefe, monga mwa
mabanja ao. 3Koma Tselofekadi, mwana wa Hefere, mwana wa
Gileadi, mwana wa Makiri, mwana wa Manase, analibe ana amuna
koma ana akazi ndiwo; ndipo maina a ana ace akazi ndiwo: Mala,
ndi Nowa, Hogila, Milika ndi Tiriza. 4Ndipo anayandikira pamaso pa
Eleazare wansembe, ndi pamaso pa Yoswa mwana wa Nuni, ndi
pamaso pa akalonga, ndi kuti, Yehova analamulira Mose atipatse
colowa pakati pa abale athu; cifukwa cace anawapatsa monga
mwa lamulo La Yehova, colowa pakati pa abale a atate wao. 5Ndipo
anamgwera Manase magawo khumi, osawerenga dziko la Gileadi
ndi Basana lokhala tsidya lija la Yordano: 6popeza ana akazi a
Manase adalandira colowa pakati pa ana ace amuna; ndi dziko la
Gileadi linakhala la ana a Manase otsala. 7Ndipo malire a Manase
anayambira ku Aseri, kumka ku Mika-metatu, wokhala cakuno ca
Sekemu; namuka malire ku dzanja lamanja kwa nzika za
Enitapua. 8Dziko la Tapua linali la Manase; koma Tapua mpaka
malire a Manase linakhala la ana a Efraimu. 9Natsikira malire ku
mtsinje wa Kana, kumwera kwa mtsinje; midzi iyi inakhala ya
Efraimu pakati pa midzi ya Manase; ndi malire a Manase anali
kumpoto kwa mtsinje; ndimaturukiro ace anali
kunyanja; 10kumwera nkwa Efraimu ndi kumpoto nkwa Manase, ndi
malire ace ndi nyanja; ndi kumpoto anakomana ndi Aseri, ndi
kum'mawa anakomana ndi Isakara. 11Ndipo m'Isakara ndi m'Aseri
Manase anali nao Betiseani ndi midzi yace, ndi Ibleamu ndi midzi
yace, ndi nzika za Doro ndi midzi yace, ndi nzika za Eni-doro ndi
midzi yace, ndi nzika za Taanaki ndi midzi yace, ndi nzika za
Megido ndi midzi yace; dziko la mapiri atatu. 12Koma ana a Manase
sanatha kuingitsa a m'midzi aja, popeza Akananjanafuna kukhala
m'dziko lija. 13Ndipo kunali pamene ana a lsrayeli atakula
mphamvu anasonkhetsa Akanani osawaingitsa onse.
14Pamenepo ana a Yosefe ananena ndi Yoswa, ndi kuti,
Watipatsiranji colowa cathu camaere cimodzi ndi gawo limodzi,
popeza ife ndife anthu aunyinji, pakuti Yehova anatidalitsa ndi
pano pomwe? 15Ndipo Yoswa ananena nao, Ngati muli anthu
aunyinji, kwerani kuli mitengoko, ndi kudziswera minda m'dziko la
Aperizi ndi la Arefai; akakuceperani malo ku phiri la

Efraimu. 16Ndipo ana a Yosefe anati, Kuphiriko sikudzatifikira; ndipo
Akananionse akukhala m'dziko la cigwa ali nao magareta acitsulo,
iwo akukhala m'Bete-Seani, ndi midzi yace ndi iwo omwe akukhala
m'cigwa ca Yezereli. 17Ndipo Yoswa ananena kwa iwo a m'nyumba
ya Yosefe, kwa Efraimu ndi Manase, ndi kuti, Inu ndinu anthu
aunyinji, muli nayo mphamvu yaikuru; simudzakhala nalo gawo
limodzi lokha; 18koma kuphiriko kudzakhala kwanu pakuti
pangakhale mpa mitengo, mudzisweretu minda, ndi maturukiro
ace adzakhala anu; pakuti mudzaingitsa Akanani angakhale ali nao
magareta acitsulo, angakhale ali amphamvu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Autsa cihema ku Silo

1Ndipo msonkhano wonse wa ana a Israyeli unasonkhana ku Silo,
nuutsa komweko cihema cokomanako; ndipo dziko
linawagoniera. 2Ndipo anatsala mwa ana a Israyeli mapfuko asanu
ndi awiri osawagawira colowa cao. 3Ndipo Yoswa anati kwa ana a
Israyeli, Mucedwa mpaka liti kulowa ndi kulandira dziko limene
Yehova Mulungu wa makolo anu anakupatsani? 4Mudzifunire
amuna, pfuko liri lonse amuna atatu; kuti ndiwatume, anyamuke,
nayendeyende iwo pakati pa dziko, nalilembe monga mwa colowa
cao; nabwereoso kwa ine. 5Ndipo adzaligawa magawo asanu ndi
awiri; Yuda adzakhala m'malire ace kumwela, ndi a m'nyumba ya
Yosefe adzakhala m'malire mwao kumpoto. 6Ndipo muzilemba
dziko likhale magawo asanu ndi awiri, ndi kubwera nao kuno kwa
ine malembo ace; ndipo ndidzakuloterani maere pane pamaso pa
Yehova Mulungu wathu. 7Pakuti Alevi alibe gawo pakati pa inu;
pakuti unsembe wa Yehova ndiwo colowa cao. Koma Gadi, ndi
Rubeni, ndi pfuko la Manase logawika pakati adalandira colowa cao
tsidya lija la Yordano kum'mawa, cimene Mose mtumiki wa Yehova
adawapatsa. 8Ndipo amunawo ananyamuka, namuka; ndipo Yoswa
analamulira opita kulemba dzikowo, ndi kuti, Mukani,
muyendeyende pakati pa dziko, ndi kulilemba, oimubwerenso kwa
ine, ndipo ndidzakuloterani maere pane pamaso pa Yehova pa
Silo. 9Namuka amunawo, napitapita pakati pa dziko, nalilemba
m'buku, nayesa midzi yace, magawo asanu, nabwera kwa Yoswa
ku cigono ku Silo. 10Ndipo Yoswa anawalotera maere ku Silo
pamaso pa Yehova; ndi apo Yoswa anawagawira ana a Israyeli
dziko, monga mwa magawo ao.

Malire a Benjamini

11Ndipo maere a ana a Benjamini anakwera monga mwa mabanja
ao; ndi malire a gawo lao anaturuka pakati pa ana a Yuda ndi ana a
Yosefe. 12Ndipo malire ao a kumpoto anacokera ku Yordano; ndi
malire anakwera ku mbali ya Yeriko kumpoto, nakwera pakati pa
mapiri kumadzulo; ndi maturukiro ace anali ku cipululu ca Beti-
aveni. 13Ndipo malire anapitirirapo kumka ku Luzi, ku mbali ya
Luzi, momwemo ndi Beteli, kumwela; ndi malire anatsikira kumka
ku Atarotu-adara, ku phiri lokhala kumwela kwa Betihoroni wa
kunsi. 14Ndipo malire analembedwa nazungulira ku mbali ya
kumadzulo kumka kumwela, kucokera ku phiri pokhala patsogolo
pa Beti-horoni, kumwela kwace; ndi maturukiro ace anali ku
Kiriyatibaala, womwewo ndi Kiriyati-Yearimu, mudzi wa ana a Yuda;
ndiyo mbali ya kumadzulo. 15Ndipo mbali ya kumwela inayambira
polekezera Kiriyati-Yearimu; naturuka malire kumka kumadzulo,
naturuka kumka ku citsime ca madzi a Nefitoa; 16natsikira malire

kumka polekezera phiri lokhala patsogolo pa cigwa ca mwana wa Hinomu, ndico ca m'cigwa ca Refai kumpoto; natsikira ku cigwa ca Hinomu, ku mbali ya Ayebusi kumwela, natsikira ku Enirogeli; 17nalembedwa kumka kumpoto, naturuka ku Eni-semesi, naturuka ku Gelilotu, ndiwo pandunji pokwerera pa Adumi; natsikira ku mwala wa Bohani mwana wa Rubeni; 18napitirira ku mbali ya pandunji pa Araba kumpoto, natsikira kumka ku Araba; 19napitirira malire kumka ku mbali ya Beti-hogila kumpoto; ndi maturukiro ace a malire anali ku nyondo ya kumpoto ya Nyanja ya Mcere; pa kulekezera kwa kumwela kwa Yordano; ndiwo malire a kumwera. 20Ndipo malireace mbali ya kum'mawa ndiwo Yordano, ndico colowa ca ana a Benjamini, kunena za malire ace pozungulira pace, monga mwa mabanja ao. 21Koma midzi ya pfuko la ana a Benjamini monga mwa mabanja ao ndiyo Yeriko, ndi Beti-hogila, ndi Emekikozizi; 22ndi Beti-araba, ndi Zemaraimu, ndi Beteli; 23ndi Arimu ndi Para, ndi Ofira; 24ndi Kefaraamoni, ndi Ofini, ndi Geba; midzi khumi ndi iwiri pamodzi ndi miraga yao; 25Gibeoni ndi Rama, ndi Beeroti; 26ndi Mizipe, ndi Kefira, ndi Moza; 27ndi Rekemu, ndi Iripeeli ndi Tarala; 28ndi Zela, Elefi, ndi Yebusi, womwewo ndi Yerusalemu, Gibeati ndi Kiriyati; midzi khumi ndi inai pamodzi ndi miraga yace, Ndico colowa ca ana a Benjamini monga mwa mabanja ao.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Malire a Simeoni

1Ndipo maere aciwiri anamturukira Simeoni, pfuko la ana a
Simeoni monga mwa mabanja ao; ndi colowa cao cinali pakati pa
colowa ca ana a Yuda. 2Ndipo anali naco colowa cao Beeri-seba,
kapena Seba, ndi Molada; 3ndi Hazarasuala, ndi Bala, ndi
Ezemu; 4ndi Elitoladi, ndi Betuli, ndi Horimu; 5ndi Zikilaga, ndi Beti-
malikabotu, ndi Hazari-susa: 6ndi Beti-lebaotu, ndi Saruheni; midzi
khumi ndi itatu ndi miraga yao; 7Aini, Rimoni ndi Eteri ndi Asana;
midzi inai ndi miraga yao; 8ndi miraga yonse yozungulira midzi iyi
mpaka Baalata-beeri ndiwo Rama kumwera. Ndico colowa ca pfuko
la ana a Simeoni, monga mwa mabanja ao. 9M'gawo la ana a Yuda
muli colowa ca ana a Simeoni; popeza gawo la ana a Yuda
linawacurukira; cifukwa cace ana a Simeoni anali naco colowa
pakati pa colowa coo.

Malire a Zebuloni

10Ndipo maere acitatu anakwecera ana a Zebuloni monga mwa
mabanja ao; ndi malire a colowa cao anafikira ku Saridi; 11nakwera
malire ao kumka kumadzulo ndi ku Marala nafikira ku Dabeseti,
nafikira ku mtsinje wa patsogolo pa Yokineamu; 12ndi kucokera ku
Saridi anazungulira kumka kum'mawa kumaturukira dzuwa, mpaka
malire a Kisilotu-tabori; naturuka kumka ku Daberati, nakwera ku
Yafia; 13ndi pocoka pamenepo anapitirira kumka kum'mawa ku
Gati-heferi, ku Etikazini; naturuka ku Remoni umene ulembedwa
mpaka ku Nea, 14nauzungulira malire kumpoto, kumka ku
Hanatoni; ndi maturukiro ace anali ku cigwa ca Ifita-eli; 15ndi Kata,
ndi Nahalala ndi Simironi, ndi Idala ndi Betelehemu: midzi khumi
ndi iwiri ndi miraga yao. 16Ici ndi colowa ca ana a Zebuloni monga
mwa mabanja ao, midzi iyi ndi miraga yao.

Malire a Isakara

17Maere acinai anamturukira Isakara, kunena za ana a Isakara
monga mwa mabanja ao. 18Ndi malire ao anali ku Yezireeli, ndi
Kesulotu, ndi Sunemu; 19ndi Hafaraimu, ndi Sioni, ndi
Anaharati; 20ndi Rabiti ndi Kisioni, ndi Ebezi; 21ndi Remeti ndi Eni-
ganaimu ndi Eni-hada, ndi Beti-Pazezi; 22ndi malire anafikira ku
Tabori, ndi Sahazuma, ndi Betesemesi; ndi maturukiro a malire ao
anali ku Yordano; midzi khumi ndi isanu ndi umodzi ndi miraga
yao. 23Ici ndi colowa ca pfuko la ana a Isakara, monga mwa
mabanja ao, midzi ndi miraga yao.

Malire a Aseri

24Ndipo maece acisanu analiturukira pfuko la ana a Aseri monga
mwa mabanja ao. 25Ndi malire ao ndiwo Helikati, ndi Hali, ndi
Beteni ndi Akisafu; 26ndi Alameleki, ndi Amadi, ndi Misali; nafikira
ku Karimeli kumadzulo ndi ku Sihorilibinati; 27nazungulira

koturukira dzuwa ku Beti-dagoni, nafikira ku Zebuloni ndi ku cigwa ca Ifita-eli, kumpoto ku Beti-emeki, ndi Nehieli; naturukira ku Kabulu kulamanzere, 28ndi Ebroni, ndi Rehobo, ndi Hamoni, ndi Kana, mpaka ku Sidoni wamkuru; 29nazungulira malice kumka ku Rama, ndi ku mudzi wa linga la Turo; nazungulira malire kumka ku Hosa; ndi maturukiro ace anali kunyanja, kucokera ku Hebeli mpaka ku Akizibu; 30Uma womwe ndi Afeki, ndi Rehobo; midzi makumi awiri mphambu iwiri ndi miraga yao, 31Ici ndi colowa ca pfuko la ana a Aseri monga mwa mabanja ao, midzi iyi ndi miragayao.

Malire a Nafitali

32Maere acisanu ndi cimodzi anaturukira ana a Nafitali, ana a Nafitali monga mwa mabanja ao. 33Ndipo malire ao anayambira ku Helefi, ku thundu wa ku Zaanani, ndi Adaminekebi, ndi Yabineeli, mpaka ku Lakumu; ndi maturukiro ace anali ku Yordano; 34nazungulira malire kumka kumadzulo ku Azinotu-tabori, naturukira komweko kumka ku Hukoku; nafikira ku Zebuloni kumwera, nafikira ku Aseri kumadzulo, ndi ku Yuda pa Yordano kum'mawa. 35Ndipo midzi yamalinga ndiyo Zidimu, Zeri, ndi Hamati, Rakati, ndi Kinereti; 36ndi Adama, ndi Rama, ndi Hazori; 37ndi Kedesi, ndi Edrei, ndi Eni-hazori; 38ndi Ironi, ndi Migidala-eli, Horemu, ndi Betianati, ndi Beti-semesi; midzi khumi ndi isanu ndi inai, ndi miraga yao. 39Ici ndi colowa ca pfuko la ana a Nafitali, monga mwa mabanja ao, midzi ndi miraga yao.

Malire a Dani

40Maere acisanu ndi ciwiri anaturukira pfuko la ana a Dani, monga mwa mabanja ao. 41Ndipo malire a colowa cao anali Zora, ndi Esitaoli ndi Iri-semesi; 42Saalabini, ndi Aijaloni ndi ltila; 43ndi Eloni ndi Timna ndi Ekroni; 44ndi Eliteke, ndi Gibetoni, ndi Baalati; 45ndi Yehudi, ndi Bene-beraki, ndi Gatirimoni; 46ndi Me-jarikoni, ndi Rakoni, ndi malire pandunji pajapo. 47Koma malire a ana a Dani anaturuka kupitirira iwowa; pakuti ana a Dani anakwera nathira nkhondo ku Lesemu, naulanda naukantha ndi lupanga lakuthwa, naulandira, nakhala m'mwemo, naucha Lesemu, Dani; ndilo dzina la Dani atate wao. 48Ici ndi colowa ca pfuko la ana a Dani, monga mwa mabanja ao, midzi iyi ndi miraga yao.

Colowa ca Yoswa

49Ndipo atatha kuligawa dziko likhale colowa cao monga mwa malire ace, ana a Israyeli anapatsa Yoswa mwana wa Nuni colowa pakati pao; 50monga mwa lamulo la Yehova anampatsa mudzi umene anawapempha, ndiwo Timinatisera, ku mapiri a Efraimu; ndipo anamangamudziwonakhala m'mwemo.

51Izi ndizo zolowa anazigawa Eleazare wansembe, ndi Yoswa mwana wa Nuni, ndi akulu a nyumba za atate a mapfuko a ana a

Israyeli, zikhale zao zao, ndi kulota maere ku Silo pamaso pa Yehova ku khomo la cihema cokomanako. Momwemo anatha kuligawa dziko.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Midzi yopulumukirako

1Ndipo Yehova anati kwa Yoswa, 2Nena ndi ana a Israyeli ndi kuti,
Mudziikire midzi yopulumukirako, monga ndinanena kwa inu mwa
dzanja la Mose, 3kuti athawireko wakupha munthu osamupha dala,
osadziwa; ndipo idzakhalira inu yopulumukirako, kumpulumuka
wolipsa mwazi. 4Munthu akathawira umodzi wa midzi iyi, aziima
polowera pa cipata ca mudziwo, nafotokozere mlandu wace
m'makutu a akuru a mudziwo; pamenepo azimlandira kumudzi
kwao, ndi kumpatsa malo, kuti akhale pakati pao. 5Ndipo
akamlondola wolipsa mwazi, asampereke m'dzanja lace wakupha
mnzaceyo; pakuti anakantha mnansi wace mosadziwa, osamuda
kale. 6Ndipo azikhala m'mudzimo mpaka adzaima pamaso pa
msonkhano anene mlandu wace, mpaka atafa mkulu wansembe
wa m'masiku omwewo; pamenepo wakupha mnzace azibwerera
ndi kufika kumudzi kwace, ndi nyumba yace, kumudzi kumene
adathawako. 7Ndipo anapatula Kedesi m'Galileya ku mapiri a
Nafitali, ndi Sekemu ku mapiri a Efraimu, ndi mudzi wa Ariba ndiwo
Hebroni ku mapiri a Yuda. 8Ndipo tsidya lija la Yordano kum'mawa
kwa Yeriko, anaika Bezeri m'cipululu, kucidikha, wa pfuko la
Rubeni, ndi Ramoti m'Gileadi wa ofuko la Gadi, ndi Golani
m'Basana wa pfuko la Manase. 9Iyi ndi midzi yoikidwira ana onse a
Israyeli, ndi mlendo wakukhala pakati pao, kuti athawireko ali
yense wakupha munthu, ndi kuti asafe ndi dzanja la wolipsa
mwazi, asanaime pamaso pa msonkhano.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Midzi yokhalamo Alevi

1Pamenepo akuru a nyumba za atate a Alevi anayandikira kwa
Eleazare wansembe, ndi kwa Yoswa mwana wa Nuni, ndi kwa
akuru a nyumba za atate a mapfuko a ana a Israyeli; 2nanena nao
ku Silo m'dziko la Kanani, ndi kuti Yehova analamulira mwa dzanja
la Mose kuti atipatse midzi yokhalamo ife, ndi mabusa a zoweta
zathu. 3Ndipo ana a Israyeli anapatsa Alevi, kutapa pa colowa cao,
monga mwa lamulo la Yehova, midzi iyi ndi mabusa ao.
4Ndipo maere anaturukira mabanja a Akohati; ndipo molota maere
ana a Aroni wansembe, ndiwo Alevi, analandira motapa pa pfuko la
Yuda, ndi pa pfuko la Simeoni, ndi pa pfuko la Benjamini, midzi
khumi ndi itatu.
5Ndipo ana otsala a Kohati analandira molota maere motapa pa
mabanja a pfuko la Efraimu, ndi pa pfuko La Dani, ndi pa pfuko La
Manase logawika pakati, midzi khumi.
6Ndipo ana a Gerisoni analandira molota maere motapa pa
mabanja a pfuko la Isakara, ndi pa pfuko la Aseri, ndi pa pfuko la
Nafitali, ndi pa pfuko la Manase logawika pakati m'Basana, midzi
khumi ndi itatu.
7Ana a Merari, monga mwa mabanja ao, analandira motapa pa
pfuko la Rubeni, ndi pa pfuko la Gadi, ndi pa pfuko la Zebuloni
midzi khumi ndi iwiri.
8Motero ana a Israyeli anapatsa Alevi midzi iyi ndi mabusa ao,
molota maere, monga Yehova adalamulira mwa dzanja la
Mose. 9Ndipo anapatsa motapa pa pfuko la ana a Yuda, ndi pa
pfuko la ana a Simeoni, midzi iyi yochulidwa maina ao; 10kuti
ikhale ya ana a Aroni a mabanja a Akohati, a ana a Levi, pakuti
maere oyamba adaturukira iwowa. 11Ndipo anawapatsa mudzi wa
Ariba, ndiye atate wa Anoki, womwewo ndi Hebroni, ku mapiri a
Yuda, ndi mabusa ace ozungulirapo. 12Koma minda ya mudzi ndi
miraga yace anapatsa Kalebe mwana wa Yefune, ikhale yace.
13Ndipo kwa ana a Aroni wansembe anapatsa Hebroni ndi mabusa
ace, ndiwo mudzi wopulumukirako wakupha mnzace, ndi Libina ndi
mabusa ace; 14ndi Yatiri ndi mabusa ace, ndi Esitimoa ndi mabusa
ace; 15ndi Holoni ndi mabusa ace, ndi Debiri ndi mabusa ace; 16ndi
Aini ndi mabusa ace, ndi Yuta ndi mabusa ace, ndi Betisemesi ndi
mabusa ace; midzi isanu ndi inai yotapira mapfuko awiri
aja. 17Ndipo motapira pfuko La Benjamini, Gibeoni ndi mabusa ace,
Geba ndi mabusa ace, 18Anatotu ndi mabusa ace, ndi Alimoni ndi
mabusa ace; midzi inai. 19Miclzi yonse ya ana a Aroni, ansembe,
ndiyo khumi ndi itatu, ndi mabusa ao.
20Ndipo mabanja a ana a Kohati, Aleviwo, otsala a ana a Kohati,
analandira midzi ya maere ao motapira pa pfuko la

Efraimu. 21Ndipo anawapatsa Sekemu ndi mabusa ace ku mapiri a Efraimu, ndiwo mudzi wopulumukirako wakupha mnzaceyo, ndi Gezeri ndi mabusa ace; 22ndi Kibizaimu ndi mabusa ace, Betihoroni ndi mabusa ace; midzi inai. 23Ndipo motapira m'pfuko La Dani, Eliteke ndi mabusa ace, Gibetoni ndi mabusa ace; 24Aijaloni ndi mabusa ace, Gati-rimoni ndi mabusa ace; midzi inai. 25Ndipo motapira pa pfukola Manaselogawika pakati, Taanaki ndi mabusa ace, ndi Gati-rimoni ndi mabusa ace; midzi iwiri. 26Midzi yonse ya mabanja a ana otsala a Kohati ndiyo khumi ndi mabusa ao.
27Ndipo anapatsa ana a Gerisoni, a mabanja a Alevi, motapira pa pfuko la Manase logawika pakati, Golani m'Basana ndi mabusa ace, ndiwo mudzi wopulumukirako wakupha mnzaceyo; ndi Beesitera ndi mabusa ace; midzi iwiri. 28Ndipo motapira pa pfuko la Isakara, Kisioni ndi mabusa ace, Daberati ndi mabusa ace; 29Yarimutu ndi mabusa ace, Eniganimu ndi mabusa ace; midzi inai. 30Ndipo motapira pa pfuko La Aseri, Misali ndi mabusa ace, Abidoni ndi mabusa ace; 31Helikati ndi mabusa ace, ndi Rehobo ndi mabusa ace; midzi inai. 32Ndipo motapira pa pfuko la Nafitali, Kedesi m'Galileya ndi mabusa ace, ndiwo mudzi wopulumukirako wakupha mnzaceyo, ndi Hamotidori ndi mabusa ace, ndi Karitani ndi mabusa ace, midzi itatu. 33Midzi yonse ya Agerisoni monga mwa mabanja ao ndiyo midzi khumi ndi itatu ndi mabusa ao.
34Ndipo anapatsa kwa mabanja a ana a Merari, otsala a Alevi, motapira pa pfuko la Zebuloni, Yokineamu ndi mabusa ace, ndi Karita ndi mabusa ace, 35Dimna ndi mabusa ace, Nahalala ndi mabusa ace; midzi inai. 36Ndipo motapira pa pfuko la Rubeni, Bezeri ndi mabusa ace, ndi Yahazi ndi mabusa ace, 37Kedimotu ndi mabusa ace, ndi Mefati ndi mabusa ace; midzi inai. 38Ndipo motapira m'pfuko la Gadi, Ramoti m'Gileadi ndi mabusa ace ndiwo mudzi wopulumukirako wakupha mnzaceyo, ndi Mahanaimu ndi mabusa ace; 39Hesiboni ndi mabusa ace. Yazeri ndi mabusa ace: yonse pamodzi midzi inai. 40Yonseyi ndiyo midzi ya ana a Merari monga mwa mabanja ao, ndiwo otsala a mabanja a Alevi; ndipo gawo lao ndilo midzi khumi ndi iwiri.
41Midzi yonse ya Alevi, pakati pa colowa ca ana a Israyeli ndiyo midzi makumi anai kudza isanu ndi itatu, ndi mabusa ao. 42Midzi iyi yonse inali nao mabusa ao pozungulira pao: inatero midzi iyi yonse.
43Motero Yehova anawapatsa Israyeli dziko lonse adalumbiralo kuwapatsa makolo ao: ndipo analilandira lao lao, nakhala m'mwemo. 44Ndipo Yehova anawapatsa mpumulo pozungulira ponse, monga mwa zonse adalumbirira makolo ao; ndipo pamaso pao sipanaima munthu mmodzi wa adani ao onse; Yehova anapereka adani ao onse m'manja mwao. 45Sikadasowa kanthu

konse ka zinthu zokoma zonse Yehova adazinenera nyumba ya Israyeli; zidacitika zonse.

©The Bible Society of Malawi, 1992

A pfuko la Rubeni, la Gadi, ndi la Manase logawika pakati, amuka kwao kum'mawa kwa Yordano

1Pamenepo Yoswa anaitana Arubeni ndi Agadi, ndi pfuko la Manase
logawika pakati, 2nanena nao, Mwasunga inu zonsezo
anakulamulirani Mosemtumiki wa Yehova; mwamveranso mau
anga m'zonse ndinakulamulirani inu; 3simunasiya abale anu
masiku awa ambiri mpaka lero lino, koma mwasunga cisungire
lamulola Yehova Mulungu wanu. 4Ndipo tsopano Yehova Mulungu
wanu wapumitsa abale anu, monga adanena nao; potero
bwererani tsopano, mu kani ku mahema anu, ku dziko la colowa
canu cimene Mose mtumiki wa Yehova anakuninkhani tsidya lija la
Yordano. 5Koma samalirani bwino kuti mucite cilangizo ndi cilamulo
zimene Mose mtumiki wa Yehova anakulamulirani kukonda Yehova
Mulungu wanu, ndi kuyenda m'njira zace zonse ndi kusunga
malamulo ace, ndi kumuumirira iye, ndi kumtumikira iye ndi mtima
wanu wonse ndi moyo wanu wonse. 6Momwemo Yoswa
anawadalitsa, nawauza amuke; ndipo anamuka ku mahema
ao. 7Ndipo gawo limodzi la pfuko la Manase, Mose anawapatsa
colowa m'Basana; koma gawo lina Yoswa anawaninkha colowa
pakati pa abale ao tsidya lija la Yordano kumadzulo. Ndiponso
pamene Yoswa anawauza amuke ku mahema ao,
anawadalitsa; 8nanena nao ndi kuti, Bwererani naco cuma cambiri
ku mahema anu, ndi zoweta zambirimbiri, ndi siliva, ndi golidi, ndi
mkuwa, ndi citsulo, ndi maraya ambirimbiri; mugawane nao abale
anu zofunkha kwa adani anu.
9Ndipo ana a Rubeni, ndi ana a Gadi, ndi pfuko la Manase logawika
pakati anabwerera, nacoka kwa ana a Israyeli ku Silo, ndiwo wa
m'dziko la Kanani kumka ku dziko la Gileadi, ku dziko lao lao,
limene anakhala eni ace, monga mwa lamulo la Yehova, mwa
dzanja la Mose.

Guwa la nsembe la umboni

10Ndipo pamene anafikira mbali ya ku Yordano, ndilo la m'dziko la
Kanani, ana a Rubeni, ndi ana a Gadi, ndi pfuko la Manase
logawika pakati anamanga ku Yordano guwa la nsembe, guwa
lalikuru maonekedwe ace. 11Ndipo ana a Israyeli anamva anthu
akuti, Taonani ana a Rubeni, ndi ana a Gadi, ndi pfuko la Manase
logawika pakati anamanga guwa la nsembe pandunji pa dziko la
Kanani, ku mbali ya ku Yordano, ku mbali ya ana a
Israyeli. 12Pamene ana a Israyeli anamva ici msonkhano wonse wa
ana a Israyeli anasonkhana ku Silo, kuti awakwerere kuwathira
nkhondo.
13Ndipo ana a Israyeli anatumiza kwa ana a Rubeni, ndi ana a
Gadi, ndi pfuko la Manase logawika pakati, ku dziko la Gileadi,

Pinehasi mwana wa Eleazare wansembe, 14ndi akalonga khumi naye; nyumba imodzi ya atate kalonga mmodzi, kotero ndi mapfuko onse a Israyeli; yense wa iwowa ndiye mkuru wa nyumba ya atate ao mwa mabanja a Israyeli. 15M'mene anafika kwa ana a Rubeni, ndi ana a Gadi, ndi pfuko la Manase logawika pakati, ku dziko la Gileadi, ananena nao ndi kuti, 16Utero msonkhano wonse wa Yehova, Colakwa ici nciani mwalakwira naco Mulungu wa Israyeli, ndi kumtembenukira Yehova lero line kusamtsatanso, popeza munadzimangira guwa la nsembe kupikisana ndi Yehova lero lino? 17Kodi mphulupulu ya ku Peori iticepera, imene sitinadziyeretsera mpaka lero lino, ungakhale mliri unadzera msonkhano wa Yehova, 18kuti mubwerera lero line kusatsata Yehova? ndipo kudzakhala kuti popeza lero mupikisana ndi Yehova, mawa adzakwiyira msonkhano wonse wa Israyeli. 19Koma mukayesa dziko La colowa canu ncodetsa, olokani kulowa m'dziko lacolowaca Yehova m'mene cihemaca Yehovacikhalamo, nimukhale naco colowa pakati pa ife; koma musapikisana ndi Yehova kapena kupikisana nafe, ndi kudzimangira nokha guwa la nsembe, pamodzi ndi guwa la nsembe la Yehova Mulungu wathu. 20Kodi Akani mwana wa Zera sanalakwa m'coperekedwaco, ndipo mkwiyo unagwera msonkhano wonse wa Israyeli? osangoonongeka yekha munthuyo mu mphulupulu yace.
21Pamenepo ana a Rubeni, ndi ana a Gadi, ndi pfuko la Manase logawika pakati anayankha, nanena ndi akuru a mabanja a Israyeli, 22Yehova Cauta Mulungu, Yehova Cauta Mulungu, iye adziwa, ndi Israyeli adzadziwa; ngati mopikisana, ngati molakwira Yehova, 23tadzimangira guwa la nsembe, kubwerera kusamtsata Yehova, musatipulumutsa lero lino; kapena ngati kufukizapo nsembe yopsereza, kapena nsembe yaufa, kapena kuperekapo nsembe zoyamika, acifunse Yehova mwini wace; 24ndipo ngati ife sitinacita ici cifukwa ca kuopa mlandu, ndi kuti, Masiku akudzawo ana anu akadzanena ndi ana athu, ndi kuti, Muli ciani inu kwa Yehova Mulungu wa Israyeli? 25pakuti Yehova anaika Yordano ukhale malire pakati pa ife ndi inu, ana a Rubeni, ndi ana a Gadi; mulibe gawo ndi Yehova; motero ana anu adzaleketsa ana athu asaope. Yehova. 26Cifukwa cace tinati, Tiyeni tikonzeretu zotimangira guwa la nsembe, si kufukizapo nsembe yopsereza ai, kapena nsembe yophera ai; 27koma lidzakhala mboni pakati pa ife ndi inu; ndi pakati pa mibadwo yathu ya m'tsogolo, kuti tikacita nchito ya Yehova pamaso pace ndi nsembe zathu zopsereza, ndi zophera, ndi zoyamika; kuti ana anu asanene ndi ana athu m'tsogolomo, Mulibe gawo ndi Yehova. 28Cifukwa cace tinati, Kudzali, akadzatero kwa ife, kapena kwa mibadwo yathu m'tsogolomo, kuti tidzati, Tapenyani, citsanzo ca guwa la nsembe

la Yehova, comanga makolo athu, si kufukizapo nsembe yopsereza ai, kapena nsembe yophera ai, koma ndilo mboni pakati pa ife ndi inu. 29Sikungatheke kuti tipikisane ndi Yehova ndi kubwerera lero kusatsata Yehova, kumanga guwa la nsembe la kufukizapo nsembe yopsereza, la nsembe yaufa, kapena yophera, pamodzi ndi guwa la nsembe la Yehova Mulungu wathu lokhala pakhomo pa cihema cace.
30Pamene Pinehasi wansembe, ndi akalonga a msonkhano ndi akuru a mabanja a Israyeli okhala naye anamva mau adawanena ana a Rubeni, ndi ana a Gadi, ndi ana a Manase, anawakomera pamaso pao. 31Ndipo Pinehasi, mwana wa Eleazare wansembe ananena ndi ana a Rubeni, ndi ana a Gadi, ndi ana a Manase, Lero lino tidziwa kuti Yehova ali pakati pa ife, pakuti simunalakwira naco Yehova; tsopano mwalanditsa ana a Israyeli m'dzanja la Yehova. 32Ndipo Pinehasi mwana wa Eleazare wansembe, ndi akalonga anabwerera kucokera kwa ana a Rubeni, ndi kwa ana a Gadi, m'dziko la Gileadi, kudza ku dziko La Kanani kwa ana a Israyeli, nawabwezera mau. 33Ndipo mauwo anakomera ana a Israyeli pamaso pao; ndi ana a Israyeli analemekeza Mulungu, osanenanso za kuwakwerera ndi kuwathira nkhondo, kuliononga dziko lokhalamo ana a Rubeni ndi ana a Gadi. 34Ndipo ana a Rubeni ndi: ana a Gadi analicha guwa la nsembelo: Ndilo mboni pakati pa ife kuti Yehova ndiye Mulungu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Yoswa acenjeza anthu asunge Malamulo a Mulungu

1Ndipo atapita masiku ambiri, Yehova atapumulitsa Israyeli kwa
adani ao onse akuwazungulira, ndipo Yoswa adakalamba nakhala
wa zaka zambiri; 2Yoswa anaitana Aisrayeli onse, akulu akulu ao,
ndi akuru ao, ndi oweruza ao, ndi akapitao ao, nanena nao,
Ndakalamba, ndine wa zaka zambiri; 3ndipo munapenya zonse
Yehova Mulungu anacitira mitundu iyi yonse ya anthu cifukwa ca
inu; pakuti Yehova Mulungu wanu ndiye anakuthirirani
nkhondo. 4Taonani, ndakugawirani mitundu ya anthu iyi yotsala
ikhale colowa ca mapfuko anu, kuyambira ku Yordano, ndi mitundu
yonse ya anthu ndinaipasula, mpaka ku nyanja yaikuru ku
malowero a dzuwa. 5Ndipo Yehova Mulungu wanu Iyeyu
adzawapitikitsa pamaso panu, ndi kulanda dziko lao kuwacotsa
pamaso panu, ndipo mudzalandira dziko lao likhale colowa canu;
monga Yehova Mulungu wanu ananena ndi inu. 6Koma mulimbike
mtima kwambiri kusunga ndi kucita zonse zolembedwa m'buku la
cilamulo ca Mose, osacipambukira kulamanja kapena
kulamanzere; 7osalowa pakati pa amitundu awa otsala mwa inu;
kapena kuchula dzina la milungu yao; osalumbiritsa nalo, kapena
kuitumikira, kapena kuigwadira; 8koma muumirire Yehova Mulungu
wanu, monga munacita mpaka lero lino. 9Pakuti Yehova anaingitsa
pamaso panu mitundu yaikuru ndi yamphamvu; koma inu, palibe
munthu anaima pamaso panu mpaka lero lino. 10Munthu mmodzi
wa inu adzapitikitsa anthu cikwi cimodzi; pakuti Yehova Mulungu
wanu ndiye amathirira inu nkhondo monga ananena ndi
inu. 11Potero mudzisamalire ndithu kuti mukonde Yehova Mulungu
wanu. 12Koma, mukadzabwereram'mbuyo pang'ono pokha ndi
kuumirira otsala a mitundu awa, ndiwo akutsala pakati pa inu, ndi
kukwatitsana nao, ndi kulowana nao, naonso kulowana
nanu; 13dziwani ndithu kuti Yehova Mulungu wanu sadzalandanso
dziko la amitundu awa kuwacotsa pamaso panu; koma adzakhala
kwa inu deka ndi msampha ndi mkwapulo m'nthiti mwanu, ndi
minga m'maso mwanu, mpaka mudzatayika m'dziko lokoma ili
anakupatsani Yehova Mulungu wanu. 14Ndipo taonani, lero lino
ndirikumuka njira ya dziko lonse lapansi; ndipo mudziwa m'mitima
yanu yonse, ndi m'moyo mwa inu nonse, kuti pa mau okoma onse
Yehova Mulungu wanu anawanena za inu sanagwa padera mau
amodzi; onse anacitikira inu, sanasowapo mau amodzi. 15Ndipo
kudzakhala kuti monga zakugwerani zokoma zonse anakunenerani
Yehova Mulungu wanu, momwemo Yehova adzakutengerani zoipa
zonse mpaka atakuonongani kukucotsani m'dziko lokoma ili
anakupatsani Yehova Mulungu wanu. 16Mukalakwira cipangano ca
Yehova Mulungu wanu cimene analamulira inu ndi kumuka ndi

kutumikira milungu yina ndi kuigwadira, mkwiyo wa Mulungu udzayakira inu, nimudzatayika msanga m'dziko lokomali anakupatsani.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Yoswa akumbutsa anthu zowacitira Mulungu

1Ndipo Yoswa anasonkhanitsa mapfuko onse a Israyeli ku Sekemu,
naitana akulu akulu a Israyeli ndi akuru ao, ndi oweruza ao, ndi
akapitao ao; ndipo anadzilangiza pamaso pa Mulungu. 2Ndipo
Yoswa ananena ndi anthu onse, Atero Yehova Mulungu wa Israyeli,
Kale lija makolo anu anakhala tsidya lija la mtsinje, ndiye Tera,
atate wa Abrahamu ndi atate wa Nahori; natumikira milungu yina
iwowa. 3Ndipo ndinamtenga kholo lanu Abrahamu tsidya lija la
mtsinje, ndi kumuyendetsa m'dziko lonse la Kanani ndi kucurukitsa
mbeu zace ndi kumpatsa Isake, 4Ndi kwa Isake ndinapatsa Yakobo
ndi Esau, ndipo ndinampatsa Esau phiri la Seiri likhale lace lace;
koma Yakobo ndi ana ace anatsikira kumka ku Aigupto. 5Pamenepo
ndinatuma Mose ndi Aroni, ndipo ndinasautsa Aigupto, monga
ndinacita pakati pace; ndipo nditatero ndinakuturutsani. 6Ndipo
ndinaturutsa atate anu m'Aigupto; ndipo munadzakunyanja; koma
Aaigupto analondola atate anu ndi magareta ndi apakavalo mpaka
ku Nyanja Yofiira. 7Ndipo pamene anapfuula kwa Yehova, anaika
mdima pakati pa inu ndi Aaigupto nawatengera nyanja, nawamiza;
ndi maso anu anapenya cocita Ine m'Aigupto; ndipo munakhala
m'cipululu masiku ambiri. 8Pamenepo ndinakulowetsani inu
m'dziko la Aamori okhala tsidya lija la Yordano; nagwirana nanu
iwowa; ndipo ndinawapereka m'dzanja lanu, nimunalandira dziko
lao likhale lanu lanu; ndipo ndinawaononga pamaso
panu. 9Pamenepo Balaki mwana wa Zipori, mfumu ya Moabu,
anauka naponyana ndi Israyeli; natuma naitana Balamu mwana wa
Beori atemberere inu; 10koma sindinafuna kumvera Balamu, potero
anakudalitsani cidalitsire, ndipo ndinakulanelitsani m'dzanja
lace. 11Pamenepo munaoloka Yordano, ndi kufika ku Yeriko; ndi eni
ace a ku Yeriko anaponyana nanu nkhondo, Aamori, ndi Aperizi, ndi
Akanani, ndi Ahiti, ndi Agirigasi, Ahivi ndi Ayebusi; ndipo
ndinawapereka m'dzanja lanu. 12Ndipo ndinatuma mabvu
atsogolere inu, amene anawaingitsa pamaso panu, ndiwo mafumu
awiri a Aamori; osati ndi lupanga lako, kapena ndi uta wako
ai. 13Ndipo ndinakupatsani dziko limene simunagwiramo nchito,
ndi midzi simunaimanga, ndipo mukhala m'mwemo; mukudya za
m'minda yamphesa, ndi minda yaazitona imene simunaioka.

Yoswa abwereza kucita pangano pakati pa Mulungu ndi anthu

14Ndipo tsopano, opani Yehova ndi kumtumikira ndi mtima
wangwiro ndi woona; nimucotse milungu imene makolo anu
anaitumikira tsidya lija la mtsinje, ndi m'Aigupto; nimutumikire
Yehova. 15Ndipo ngati kutumikira Yehova kukuipirani mudzisankhire
lero amene mudzamtumikira, kapena milungu imene anaitumikira

makolo anu okhala tsidya lija la mtsinje, kapena milungu ya Aamori amene mukhala m'dziko lao; koma ine, ndi a m'nyumba yanga, tidzatumikira Yehova. 16Ndipo anthu anayankha, nati, Sikungatheke kuti timsiye Yehova, ndi kutumikira milungu yina; 17pakuti Yehova Mulungu wathu ndi iye amene anatikweza kutiturutsa m'dziko la Aigupto ku nyumba ya akapolo, nacita zodabwiza zazikuruzo pamaso pathu, natisunga m'njira monse tidayendamo, ndi pakati pa anthu onse amene tinapita pakati pao; 18ndipo Yehova anaingitsa pamaso pathu anthu awa onse, ngakhale Aamori okhala m'dzikomo; cifukwa cace ifenso tidzatumikira Yehova, pakuti ndiye Mulungu wathu. 19Ndipo Yoswa anati kwa anthu, Simukhoza inu kutumikira Yehova pakuti ndiye Mulungu woyera, ndi Mulungu wansanje; sadzalekerera zolakwa zanu, kapena zocimwa zanu. 20Mukasiya Yehova, ndi kutumikira milungu yacilendo, adzatembenuka ndi kukucitirani coipa, ndi kukuthani, angakhale anakucitirani cokoma. 21Ndipo anthu anati kwa Yoswa, Iaitu, koma tidzatumikira Yehova. 22Ndipo Yoswa ananena ndi anthu, Inu mwadzicitira mboni inu nokha kuti mwadzisankhira Yehova kumtumikira iye. Ndipo anati, Ndife mboni. 23Ndipo tsopano, cotsani milungu yacilendo iri pakati pa inu, ndi kulozetsa mitima yanu kwa Yehova, Mulungu wa Israyeli. 24Ndipo anthu anati kwa Yoswa, Tidzamtumikira Yehova Mulungu wathu ndi kumvera mau ace. 25Motero Yoswa anacita pangano ndi anthu tsiku lija, nawaikira lemba ndi ciweruzo m'Sekemu.
26Ndipo Yoswa analembera mau awa m'buku la cilamulo ca Mulungu; natenga mwala waukuru, nauimitsa apo patsinde pa thundu wokhala pa malo opatulika a Yehova. 27Ndipo Yoswa anati kwa anthu onse, Taonani, mwala uwu udzakhala mboni yotitsutsa; pakuti udamva mau onse a Yehova amene ananena kwa ife; ndipo udzakhala mboni yotsutsa inu, mungakanize Mulungu wanu. 28Pamenepo Yoswa anauza anthu amuke, yense ku colowa cace.

Amwalira Yoswa ndi Eleazare

29Ndipo kunali, zitatha izi, Yoswa mwana wa Nuni mtumiki wa Yehova, adafa, wa zaka zana ndi khumi. 30Ndipo anamuika m'malire a colowa cace m'Timinati-sera, ndiwo ku mapiri a Efraimu kumpoto kwa phiri la Gaasi. 31Ndipo Israyeli anatumikira Yehova masiku onse a Yoswa, ndi masiku onse a akulu akulu otsala atafa Yoswa, amene anadziwa nchito yonse ya Yehova anaicitira Israyeli. 32Ndipo mafupa a Yosefe amene ana a Israyeli anakwera nao kucokera ku Aigupto anawaika ku Sekemu, pa kadziko kamene adakagula Yakobo kwa ana a Hamori atate wa Sekemu ndi kuwapatsa ndalama zana; ndipo anakhala colowa ca ana a

Yosefe. 33Eleazarenso mwana wa Aroni anafa; ndipo anamuika pa phiri la Pinehasi mwana wace, limene adampatsa ku mapiri a Efraimu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Judges

Oweruza 1

Aisrayeli aonjeza kugonjetsa Akanani

1NDIPO atafa Yoswa, ana a Israyeli anafunsira kwa Yehova ndi kuti, Adzayamba ndani kutikwerera pa Akanani kuwathira nkhondo? 2Ndipo Yehova anati, Akwere Yuda; taonani, ndapereka dzikoli m'dzanja lace. 3Ndipo Yuda ananena ndi Simeoni mkuru wace, Kwera nane ku gawo langa kuti tiwathire nkhondo Akanani; ndipo inenso ndidzamuka nawe ku gawo lako. Namuka naye Simeoni. 4Ndipo Yuda atakwera, Yehova anapereka Akanani ndi Aperizi m'dzanja lao, ndipo anakantha a iwowa anthu zikwi khumi. 5Ndipo anapeza Adoni-bezeki m'Bezeki, namthira nkhondo nakantha Akanani ndi Aperizi. 6Koma Adoni-bezeki anathawa; ndipo anampitikitsa, namgwira, namdula zala zazikuru za m'manja ndi za m'mapazi. 7Pamenepo anati Adoni-bezeki, Mafumu makumi asanu ndi awiri odulidwa zala zazikuru za m'manja ndi m'mapazi anaola kakudya kao pansi pa gome panga; monga ndinacita ine, momwemo Mulungu wandibwezera. Ndipo anadza naye ku Yerusalemu, nafa iye komweko.

8Ndipo ana a Yuda anacita nkhondo pa Yerusalemu, naulanda, naukantha ndi lupanga lakuthwa, natentha mudzi ndi moto. 9Ndipo atatero ana a Yuda anatsika kuthirana nao nkhondo Akanani akukhala kumapiri, ndi kumwela ndi kucidikha. 10Ndipo Yuda anamuka kwa Akanani akukhala m'Hebroni; koma kale dzina la Hebroni ndilo mudzi wa Ariba; ndipo anakantha Sesai, ndi Ahimani, ndi Talimai. 11Pocoka pamenepo anamuka kwa nzika za ku Dibiri, koma kale dzina la Dibiri ndilo mudzi wa Seferi. 12Ndipo Kalebe anati, iye amene akantha mudzi wa Seferi, naulanda, yemweyo ndidzampatsa Akisa mwana wanga wamkazi akhale mkazi wace. 13Ndipo Otiniyeli, mwana wa Kenazi mng'ono wa Kalebi anaulanda, ndipo anampatsa Akisa mwana wace wamkazi akhale mkazi wace. 14Ndipo kunali, m'mene anamdzera, anamkakamiza mwamuna wace kuti apemphe atate wace ampatse munda; natsika pa buru wace; ndipo Kalebe ananena naye, Ufunanji? 15Ndipo anati kwa Iye, Mundipatse dalitso; popeza mwandipatsa dziko lakumwela, ndipatsenso zitsime za madzi. Pamenepo Kalebe anampatsa zitsime za kumtunda ndi zitsime za kunsi.

16Ndipo ana a Mkeni mlamu wace wa Mose, anakwera kuturuka m'mudzi wa m'migwalangwa pamodzi ndi ana a Yuda, nalowa m'cipululu ca Yuda cokhala kumwela kwa Aradi; namuka iwo nakhala ndi anthuwo. 17Ndipo Yuda anamuka ndi Simeoni mkuru wace, nakantha Akanani akukhala m'Zefati, nauononga konse.

Koma dzina la mudziwo analicha Horima. 18Yuda analandanso Gaza
ndi malire ace, ndi Asikeloni ndi malire ace, ndi Ekroni ndi malire
ace. 19Ndipo Yehova anali ndi Yuda, iye nawaingitsa a kumapiri,
osaingitsanzika za kucigwa, popeza zinali nao magareta
acitsulo. 20Ndipo anapatsa Kalebe Hebroni monga Mose adanena;
iye nawaingitsa komweko ana amuna atatu a Anaki. 21Koma ana a
Benjamini sanaingitsa Ayebusi okhala m'Yerusalemu; koma Ayebusi
anakhala m'Yerusalemu pamodzi ndi ana a Benjamini, mpaka lero
lino.
22Ndipo anakwera iwo a m'nyumba ya Yosefe naonso kumka ku
Beteli; ndipo Yehova anakhala nao. 23Ndipo iwo a m'nyumba ya
Yosefe anatumiza ozonda ku Beteli. Koma kale dzina la mudziwo
ndilo Luzi. 24Ndipo alonda anaona munthu alikuturuka m'mudzi,
nanena naye, Utionetsetu nolowera m'mudzi, ndipo tidzakucitira
cifundo. 25Nawaonetsa polowera m'mudzi iye, naukantha mudzi
iwowa ndi lupanga lakuthwa; koma analola munthuyo ndi banja
lace lonse amuke. 26Ndipo munthuyo anamuka ku dziko la Ahiti,
namanga mudzi, naucha dzina lace Luzi; ndilo dzina lace mpaka
lero lino.

Aisrayeli aleka kugonjetsa Akanani ena

27Koma Manase sanaingitsa a ku Betiseani ndi midzi yace kapena a
Taanaki ndi midzi yace, kapena nzika za ku Dori ndi midzi yace,
kapena nzika za ku Ibleamu ndi midzi yace, kapena nzika za ku
Megido ndi midzi yace; koma Akanani anakhumba kukhala m'dziko
muja. 28Ndipo kunali, atakula mphamvu Israyeli, anasonkhetsa
Akanani, osawaingitsa onse.
29Ndipo Efraimu sanaingitsa Akanani okhala m'Gezeri; koma
Akanani anakhala m'Gezeri pakati pao, 30Zebuloni sanaingitsa
nzika za ku Kitroni, kapena nzika za ku Nahaloli; koma Akanaru
anakhala pakati pao, nawasonkhera.
31Aseri sanaingitsa nzika za ku Ako, kapena nzika za ku Sidoni,
kapena a Akalabu, kapena a Akisibu, kapena a Heliba, kapena a
Afiki, kapena a Rehobo; 32koma Aseri anakhala pakati pa Akanani
nzika za kudziko; pakuti sanawaingitsa.
33Nafitali sanaingitsa nzika za ku Beti-semesi, kapena nzika za ku
Beri-anati; koma anakhala pakati pa Akanani, nzika za kudziko;
koma nzika za ku Beti-semesi, ndi a ku Beti-anati zinawasonkhera.
34Ndipo Aamori anakankha ana a Dani akhale kumapiri pakuti
sanawalola atsikire kucigwa; 35Aamori anakhumbanso kukhala ku
phiri la Heresi, ku Ajaloni, ndi ku Saalibimu; koma dzanja la a
m'nyumba ya Yosefe linawalaka, nakhala iwo akupereka
msonkho. 36Ndipo malire a Aamori anayambira pokwerera pa
Akrabimu, pathanthwe, ndi pokwererapo.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Mngelo wa Mulungu adzudzula Aisrayeli

1Ndipo mthenga wa Yehova anakwera kucokera ku Giligala kumka
ku Bokimu. Ndipo anati, Ndinakukweretsani kucokera ku Aigupto,
ndi kulowetsa inu m'dziko limene ndinalumbirira makolo anu; ndipo
ndinati, Sindidzathyola cipangano canga nanu ku nthawi
yonse; 2ndipo inu, musamacita pangano ndi nzika za m'dziko ili;
muzigamula maguwa ao a nsembe. Koma simunamvera mau anga;
mwacicita ici cifukwa ninji? 3Cifukwa cacenso ndinati,
Sindidzawapitikitsa kuwacotsa pamaso panu; koma adzakhala
ngati minga m'nthiti zanu, ndi milungu yao idzakhalira inu
msampha. 4Ndipo kunali, pamene mthenga wa Yehova ananena
mau awa kwa ana onse a Israyeli, anthuwo anakweza mau ao,
nalira misozi. 5Potero analicha dzina la malowo Bokimu: namphera
Yehova nsembe pomwepo.

Aisrayeli alowerera atamwalira Yoswa

6Pamene Yoswa atawalola anthu amuke, ana a Israyeli anamuka,
yense ku colowa cace, dziko likhale lao lao. 7Ndipo anthuwo
anatumikira Yehova masiku onse a Yoswa ndi masiku onse a akulu
akulu otsala atafa Yoswa, amene adaona nchito yaikuru yonse ya
Yehova anaicitira Israyeli. 8Ndipo Yoswa mwana wa Nuni, mtumiki
wa Yehova anafa wa zaka zace zana ndi khumi. 9Ndipo anamuika
m'malire a colowa cace m'Timinatiheresi, ku mapiri a Efraimu,
kumpoto kwa phiri la Gaasi. 10Ndiponso mbadwo uwu wonse
unasonkhanidwa kuikidwa kwa makolo ao; nuuka mbadwo wina
pambuyo pao; wosadziwa Yehova kapena nchitoyi adaicitira
Israyeli, 11Ndipo ana a Israyeli anacita coipa pamaso pa Yehova,
natumikira Abaala; 12nasiya Yehova Mulungu wa makolo ao, amene
adawaturutsa m'dziko la Aigupto, natsata milungu yina, milungu
ya mitundu ya anthu okhala pozungulira pao, naigwadira; nautsa
mkwiyo wa Yehova. 13Ndipo anasiya Yehova, natumikira Baala ndi
Asitaroti. 14Pamenepo mkwiyo wa Yehova unayakira Israyeli, ndipo
anawapereka m'manja a ofunkha kuti awafunkhe; nawagulitsa
m'dzanja la adani ao akuwazungulira osakhozanso iwowo kuima
pamaso pa adani ao. 15Kuli konse anaturuka, dzanja la Yehova
linawakhalira moipa, monga Yehova adanena, ndi monga Yehova
adawalumbirira; nasautsika kwambiri iwowa. 16Ndipo Yehova
anautsa oweruza, amene anawapulumutsa m'dzanja la iwo
akuwafunkha. 17Koma sanamvera angakhale oweruza ao, pakuti
anamuka kupembedza milungu yina, naigwadira; anapambuka
msanga m'njira yoyendamo makolo ao, pomvera malamulo a
Yehova; sanatero iwowa. 18Ndipo pamene Yehova anawaukitsira
oweruza, Yehova anakhala naye woweruzayo, nawapulumutsa
m'dzanja la adani ao masiku onse a woweruzayo; pakuti Yehova

anagwidwa cisoni pa kubuula kwao cifukwa ca iwo akuwapsinja ndi kuwatsendereza. 19Koma kunali atafa woweruzayo anabwerera m'mbuyo, naposa makolo ao ndi kucita moipitsa, ndi kutsata milungu yina kuitumikira ndi kuigwadira, sanaleka kanthu ka macitidwe ao kapena ka njira yao yacheni. 20Ndipo mkwiyo wa Yehova unayakira Israyeli; nati Iye, Popezamtundu uwu unalakwira cipangano canga cunene ndinalamulira makolo ao, osamvera mau ansa; 21Inenso sindionjeza kuingitsa pamaso pao a mitundu yina imene Yoswa adaisiya pakufa iyeyu; 22kuti ndiyese nayo Israyeli ngati adzasunga njira ya Yehova kuyendamo monga anaisunga makolo ao, kapena iai. 23Motero Yehova analeka mitundu iyi osaiingitsa msanga, ndipo sadaipereka m'dzanja la yoswa.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Amitundu otsala akuyesa nao Aisrayeli

1Ndipo iyo ndiyo mitundu ya anthu anaisiyapo Yehova kuyesa nayo
Israyeli, ndiwo onse amene sanadziwa nkhondo zonse za
Kanani; 2cifukwa cace ndico cokha cakuti adziwitse mibadwo ya
ana a Israyeli ndi kuwaphunzitsa nkhondo, ngakhale iwo okha okha
osaidziwa konse kale; 3anasiya mafumu asanu a Afilisti ndi Akanani
onse, ndi Asidoni, ndi Ahivi okhala m'phiri la Lebano, kuyambira
phiri la Baalaherimoni mpaka polowera ku Hamati. 4Amenewo
anakhala coyesera Israyeli kuti Yehova adziwe ngati adzamvere
malamulo ace, amene analamulira makolo ao mwa dzanja la
Mose. 5Ndipo ana a Israyeli anakhala pakati pa Akanani, Ahiti, ndi
Aamori, ndi Aperizi, ndi Ahivi, ndi Ayebusi; 6nakwatira ana akazi a
iwowa, napereka ana ao akazi kwa ana amuna a iwowa natumikira
milungu yao.

Otiniyeli alanditsa Aisrayeli m'dzanja La Kusani

7Ndipo ana a Israyeli anacita coipa pamaso pa Yehova, naiwala
Yehova Mulungu wao, natumikira Abaala ndi zifanizo. 8Pamenepo
mkwiyo wa Mulungu unayakira Israyeli ndipo anawagulitsa
m'dzanja la KusaniRisataimu, mfumu ya Mesopotamiya; ndi ana a
Israyeli anatumikira Kusani-Risataimu zaka zisanu ndi
zitatu. 9Ndipo pamene ana a Israyeli anapfuula kwa Yehova,
Yehova anaukitsira ana a Israyeli mpulumutsi amene
anawapulumutsa, ndiye Otiniyeli mwana wa'Kenazi, mng'ono wace
wa Kalebe. 10Ndipo unamdzera mzimu wa Yehova, iye naweruza
Israyeli, naturuka kunkhondo; napereka Yehova Kusani-Risataimu
mfumu ya Mesapotamiya m'dzanja lace; ndi dzanja lace linamlaka
Kusani-Risataimu. 11Pamenepo dziko linapumula zaka makumi
anai; ndi Otiniveli mwana wa Kenazi anafa.

Ehudi awalanditsa m'dzanja la Egiloni

12Koma ana a Israyeli anaonjezanso kucita coipa pamaso pa
Yehova; pamenepo Yehova analimbitsa Egiloni mfumu ya Moabu pa
Israyeli, popeza anacita coipa pamaso pa Yehova. 13Ndipo
anadzisonkanitsira ana a Amoni ndi a Amaleki, namuka nakantha
Israyeli, nalanda mudzi wa m'migwalangwa nakhalamo. 14Ndipo
ana a Israyeli anatumildra Egiloni mfumu ya Moabu zaka khumi ndi
zisanu ndi zitatu. 15Koma pamene ana a Israyeli anapfuula kwa
Yehova, Yehova anawaukitsira mpulumutsi, Ehudi mwana wa Gera,
Mbenjamini, munthu wamanzere, ndipo ana a Israyeli anatumiza
mtulo m'dzanja lace Ikwa Egiloni mfumu ya Moabu. 16Ndipo Ehudi
anadzisulira lupanga lakuthwa konse konse utali wace mkono;
nalimangirira pansi pa zobvala zace pa ncafu ya
kulamanja. 17Ndipo anapereka mtulo kwa Egiloni, mfumu ya
Moabu; koma Egiloni ndiye munthu wonenepa ndithu. 18Ndipo

atatha kupereka mtulowo, anauza anthu onyamula mtulo
acoke. 19Koma iye mwini anabwerera pa mafano osema ali ku
Giligala, nati, Ndiri nao mau acinsinsi kwa inu, mfumu. Nati iye,
Khalani cete. Ndipo anaturuka onse akuimapo. 20Ndipo Ehudi
anamdzera alikukhala pa yekha m'cipinda cosanja copitidwa
mphepo, Nati Ehudi, Ndiri nao mau a Mulungu akukuuzani. Nauka
iye pa mpando wace. 21Ndipo Ehudi anaturutsa dzanja lace
lamanzere nagwira lupanga ku ncafu ya kulamanja nampyoza
m'mimba mwace; 22ndi cigumbu cace cinalowa kutsata mpeni
wace; ndi mafuta anaphimba mpeniwo, pakuti sanasolola lupanga
m'mimba mwace; nilituruka kumbuyo. 23Pamenepo Ehudi
anaturuka kukhonde namtsekera pamakomo pa cipinda cosanja
nafungulira. 24Ndipo atauruka iye, anadza aka polo ace; napenya,
ndipo taonani pamakomo pa cipinda cosanja mpofungulira; nati
iwo, Angophimba mapazi m'cipinda cace cosanja copitidwa
mphepo. 25Ndipo analindirira mpaka anacita manyazi; koma
taonani, sanatsegula pamakomo pa cipinda cosanja. Pamenepo
anatenga mfungulo natsegula; ndipo taonani, mbuye wao wagwa
pansi, wafa. 26Ndipo Ehudi anapulumuka pakucedwa iwo, napitirira
pa mafano osema, napulumuka kufikira Seira. 27Ndipo kunali,
pakufika iye anaomba lipenga ku mapiri a Efraimu; ndi ana a
Israyeli anatsika naye kucokera kumapiri, nawatsogolera
iye. 28Ndipo ananena nao, Nditsateni ine, pakuti Yehova wapereka
adani anu Amoabu m'manja mwanu. Ndipo anatsika ndi kumtsata,
natsekereza Amoabu madooko a Yordano, osalola mmodzi
aoloke. 29Ndipo anakantha Amoabu nyengo ija anthu zikwi khumi,
onsewa anthu amoyo, ndi ngwazi; ndipo sanapulumuka ndi
mmodzi yense. 30Motero anagonjetsa Moabu tsiku lija pansi pa
dzanja la Israyeli. Ndipo dziko linapumulazaka makumi asanu ndi
atatu.
31Atapita iye kunali Samagara, mwana wa Anati amene anakantha
Afilisti mazana asanu ndi limodzi ndi mtoso wa ng'ombe; nayenso
anapulumutsa Israyeli.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Debora ndi Baraki alanditsa Aisrayeli m'dzanja la Yabini

1Ndipo ana a Israyeli anaonjeza kucita coipa pamaso pa Yehova,
atafa Ehudi. 2Ndipo Yehova anawagulitsa m'dzanja la Yabini mfumu
ya Kanani, wocita ufumu ku Hazori; kazembe wace wa nkhondo
ndiye Sisera, wokhala ku Haroseti wa amitundu. 3Ndipo ana a
Israyeli anapfuula kwa Yehova; pakuti anali nao magareta acitsulo
mazana asanu ndi anai; napsinja ana a Israyeli kolimba zaka
makumi awiri.
4Ndipo Debora, mneneri wamkazi, ndiye mkazi wace wa Lapidoti,
anaweruza Israyeli nyengo ija, 5Ndipo anakhala patsinde pa
mgwalangwa wa Debora pakati pa Rama ndi Beteli ku mapiri a
Efraimu; ndi ana a Israyeli anakwera kwa iye awaweruze. 6Ndipo
anatuma, naitana Baraki mwana wa Abinoamu, acoke m'Kedesi-
Nafitali; nanena naye, Kodi Yehova Mulungu wa Israyeli
sanalamulira ndi kuti, Muka, nuluniike ku phiri la Tabori,
nuwatenge, apite nawe anthu zikwi khumi a ana a Nafitali ndi ana
a Zebuloni? 7Ndipo ndidzamkoka Sisera, kazembe wa nkhondo ya
Yabini, akudzere ku mtsinje wa Kisoni, ndi magareta ace, ndi
aunyinji ace; ndipo ndidzampereka m'dzanja lako. 8Ndipo Baraki
anati kwa iye, Ukamuka nane, ndidzamuka; ukapanda kumuka
nane, sindimuka. 9Nati iye, Kumuka ndidzamuka nawe, koma
ulendo umukawo, sudzacita nao ulemu; pakuti: Yehova adzagulitsa
Sisera m'dzanja la mkazi, Motero Debora anauka namuka ndi
Baraki ku Kedesi. 10Ndipo Baraki anaitana Zebuloni ndi Nafitali
asonkhane ku Kedesi; iye nakwera ndi anthu zikwi khumi
akumtsata; Deboranso anakwera kumka naye. 11Ndipo Heberi
Mkeni anadzisiyanitsa ndi Akeni, ndi ana a Hobabu mlamu wace wa
Mose, namanga mahema ace mpaka thundu wa m'Zaananimu,
ndiwo wa ku Kedesi. 12Ndipo anauza Sisera kuti Baraki mwana wa
Abinoamu wakwera ku phiri la Tabori. 13Pamenepo Sisera
anasonkhanitsa magareta ace onse ndiwo magareta mazana
asanu ndi anai acitsulo, ndi anthu onse okhala naye, kuyambira
Haroseti wa amitundu mpaka mtsinje wa Kisoni. 14Ndipo Debora
anati kwa Baraki, Nyamuka; pakuti ili ndi tsikuli Yehova wapereka
Sisera m'dzanja lako; sanaturuka kodi Yehova pamaso pako? Potero
Baraki anatsika ku phiri la Tabori ndi amuna zikwi khumi
akumtsata. 15Ndipo Ambuye anaononga Sisera, ndi magareta onse
ndi gulu lankhondo lonse, adi lupanga lakuthwa pamaso pa Baraki;
koma Sisera anatsika pagareta nathawa coyenda pansi. 16Koma
Baraki anatsata magareta ndi gululo mpaka Haroseti wa amitundu;
ndi gulu lonse lankhondo la Sisera linagwa ndi lupanga lakuthwa,
sanatsala munthu ndi mmodzi yense.

17Koma Sisera anathawira coyenda pansi ku hema wa Yaeli mkazi
wa Heberi Mkeni; pakuti panali mtendere pakati pa Yabini mfumu
ya Hazori, ndi nyumba ya Heberi Mkeni. 18Ndipo Yaeli anaturuka
kukomana ndi Sisera, nanena naye, Pambuka, mbuye wanga,
pambukira kwa ine kuno; usaope. Ndipo anapambukira kwa iye
kulowa m'hema, nampfunda ndi cimbwi. 19Pamenepo ananena
naye, Ndipatsetu madzi pang'ono ndimwe; popeza ndine waludzu.
Ndipo anatsegula thumba la mkaka, nampatsa amwe,
nampfunda. 20Ndipo Sisera ananena naye, Taima pakhomo pa
hema, ndipo kudzali, akadza munthu, akakufunsa akati, Pali
munthu pano kodi? Uziti, Palibe. 21Pamenepo Yaeli mkazi wa Heberi
anatenga ciciri ca hema, natenga nyundo m'dzanja lace namdzera
monyang'ama, nakhomera ciciri cilowe m'litsipa mwace;
nicinapyoza kulowa m'nthaka; popeza anali m'tulo tofa nato ndi
kulema; nafa. 22Ndipo taonani, pomlondola Sisera Barakiyo, Yaeli
anaturuka kukomana naye, Dati kwa iye, Idza kuno,
ndidzakuonetsa munthu umfunayo, Potero anamdzera, ndipo
taonani, Sisera wagwa, wafa, ndi ciciri m'litsipa
mwace. 23Momwemo Mulungu anagonjetsa tsiku lija Yabini mfumu
ya Kanani pamaso pa ana a Israyeli. 24Ndipo dzanja la ana a
Israyeli linamkabe ndi kulimbika pa Yabini mfumu ya Kanani mpaka
adamuononga Yabini mfumu ya Kanani.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Oweruza 5

Nyimbo ya Debora

1Ndipo Debora ndi Baraki mwana wa Abinoamu anayimba tsiku
lomwelo ndi kuti,
2Lemekezani Yehova
Pakuti atsogoleri m'Israyeli anatsogolera,
Pakuti anthu anadzipereka mwaufulu.
3Imvani mafumu inu; cherani makutu, akalonga inu;
Ndidzayimbira ine Yehova, inetu;
Ndidzamuyimbira nyimbo, Yehova, Mulungu wa Israyeli,
4Yehova, muja mudaturuka m'Seiri,
Muja mudayenda kucokera ku thengo la Edomu,
Dziko linanjenjemera, thambo lomwe linakha,
Inde mitambo inakha madzi.
5Mapiri anagwedezeka pamaso pa Yehova,
Sinai ili pamaso pa Yehova, Mulungu wa Israyeli.
6Masiku a Samagara, mwana wa Anati,
Masiku a Yaeli maulendo adalekeka
Ndi apanjira anayenda mopazapaza,
7Miraga idalekeka m'Israyeli, idalekeka.
Mpaka ndinauka ine Debora,
Ndinauka ine amai wa Israyeli.
8Anasankha milungu yatsopano,
Pamenepo nkhondo inaoneka kuzipata.
Ngati cikopa kapena nthungo zidaoneka
Mwa zikwi makumi anai a Israyeli?
9Mtima wanga ubvomerezana nao olamulira a m'Israyeli,
Amene anadzipereka mwaufulu mwaanthu.
Lemekezani Yehova.
10Inu akuyenda okwera pa aburu oyera,
Inu akukhala poweruzira,
Ndi inu akuyenda m'njira, fotokozerani.
11Posamveka phokoso la amauta potunga madzi,
Pomwepo adzafotokozera zolungama anazicita Yehova,
Zolungama anazicita m'miraga yace, m'Israyeli.
Pamenepo anthu a Yehova anatsikira kuzipata.
12Galamuka, Debora, galamuka,
Galamuka, galamuka, unene nyimbo;
Uka, Baraki, manga nsinga ndende zako, mwana wa Abinoamu, iwe.
13Pamenepo omveka otsala anatsika ndi anthu;
Yehova ananditsikira pakati pa acamuna.
14Anafika Aefraimu amene adika mizu m'Amaleki;
Benjamini anakutsata iwe pakati pa anthu ako.
Ku Makiri kudacokera olamulira,

Ndi ku Zebuloni iwo akutenga ndodo ya mtsogoleri.
15Akalonga a Isakara anali ndi Debora;
Monga Isakara momwemo Baraki,
Anawatuma m'cigwa namka coyenda pansi.
Pa mitsinje ya Rubeni panali zotsimikiza mtima zazikuru.
16Wakhaliranji pakati pa makola,
Kumvera kulira kwa zoweta?
Ku timitsinje ta Rubeni kunali zotsimikiza mtima zazikuru.
17Gileadi anakhala tsidya lija la Yordano;
Ndi Dani, akhaliranji mzombo?
Aseri anakhala pansi m'mphepete mwa nyanja,
Nakhalitsa pa nyondo yace ya nyanja.
18Zebuloni ndiwo anthu anataya moyo wao mpaka imfa,
Nafitali yemwe poponyana pamisanje.
19Anadza mafumu, nathira nkhondo
Pamen'epo anathira nkhondo mafumu a Kanani.
M'Taanaki, ku madzi a Megido;
Osatengako phindu la ndarama.
20Nyenyezi zinathira nkhondo yocokera kumwamba,
M'mipita mwao zinathirana ndi Sisera.
21Mtsinje wa Kisoni unawakokolola,
Mtsinje uja wakale, mtsinje wa Kisoni.
Yenda mwamphamvu, moyo wangawe.
22Pamenepo ziboda za akavalo zinaguguda,
Ndi kutumphatumpha, kurumphatumpha kwa anthu ace eni mphamvu,
23Mutemberere Merozi, ati mthenga wa Yehova,
Mutemberere citemberere nzika zace;
Pakuti sanadzathandiza Yehova,
Kumthandiza Yehova pa acamuna.
24Wodalitsika, woposa akazi, akhale Yaeli
Mkazi wa Heberi Mkeni.
Akhale wodalitsika woposa akazi a m'hema.
25Mwamunayo anapempha madzi, anampatsa mkaka,
Anamtengera mafuta a mkaka m'cotengera ca mfulu.
26Dzanja lace analitambasulira kuciciri,
Ndi dzanja lace lamanja ku nyundo ya anchito,
Nakhomera Sisera, nakantha mutu wace,
Inde, anaphwanya napyoza m'litsipa mwace.
27Pa mapazi ace anabzong'onyoka, anagwa, anagona;
Pa mapazi ace anabzong'onyoka, anagwa;
Pobzong'onyokapo, pamenepo wagwa wafa.
28Anapenyerera ali pazenera, napfuula
Mace wa Sisera, pa made ace,

Acedweranji gareta wace?
Zizengerezeranji njinga za magareta ace?
29Akazi anzace omveka anzeru anamyankha;
Koma anadziyankhira yekha mau,
30Kodi sanapeza, sanagawa zofunkha?
Namwali, anamwali awiri kwa munthu ali yense.
Cofunkha ca nsaru za mawanga mawanga kwa Sisera;
Cofunkha ca nsaru za mawanga mawanga, za maluwa,
Nsaru za mawanga mawanga, za maluwa konse konse, kwa cofunkha ca khosi lace.
31Adani anu onse, Yehova, atayike momwemo.
Koma iwo akukonda Inu akhale ngati dzuwa loturuka mu mphamvu yace.
Ndipo dziko linapumula zaka makumi anai.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Midyani agonjetsa Aisrayeli

1Koma ana a Israyeli anacita coipa pamaso pa Yehova; ndipo
Yehova anawapereka m'dzanja la Midyani zaka zisanu ndi
ziwiri. 2Pamene dzanja la Midyani linalaka Israyeli, ana a Israyeli
anadzikonzera ming'ang'ala ya m'mapiri, ndi mapanga, ndi
malinga cifukwa ca Midyani. 3Ndipo kunali, akabzala Israyeli,
amakwera Amidyani, ndi Amaleki, ndi ana a kum'mawa, inde
amawakwerera; 4nawamangira misasa, namaononga zipatso za
m'dziko mpaka ufika ku Gaza, osawasiyira cocirira njala m'Israyeli,
ngakhale nkhosa, kapena ng'ombe, kapena buru. 5Pakuti anakwera
nazo zoweta zao ndi mahema ao, analowa ngati dzombe kucuruka
kwao; iwowa ndi ngamila zao zomwe nzosawerengeka; ndipo
analowa m'dziko kuliononga. 6Ndipo Israyeli anafoka kwambiri
cifukwa ca Midyani; ndipo ana a Israyeli anapfuula kwa Yehova.
7Ndipo kunali, pamene ana a Israyeli anapfuula kwa Yehova
cifukwa ca Midyani, 8Yehova anatuma munthu mneneri kwa ana a
Israyeli, nanena nao, Atero Yehova Mulungu wa Israyeli, Ine
ndinakukwezani kucokera m'Aigupto, ndi kukuturutsani m'nyumba
ya ukapolo; 9ndipo ndinakulanditsani m'dzanja la Aaigupto, ndi
m'dzanja la onse akupsinja inu, ndi kuwaingitsa pamaso panu, ndi
kukupatsani dziko lao; 10ndipo ndinati kwa inu, Ine ndine Yehova
Mulungu wanu; musamaopa milungu ya Aamori amene mukhala
m'dziko lao; koma simunamvera mau anga.

Mngelowa Mulungu amdzera Gideoni

11Pamenepo anadza mthenga wa Yehova, nakhala patsinde pa
thundu wokhala m'Ofira, wa Yoasi M-abieziri; ndi mwana wace
Gideoni analikuomba tirigu m'mopondera mphesa, awabisire
Amidyani. 12Ndipo mthenga wa Yehova anamuonekera, nati kwa
iye, Yehova ali nawe, ngwazi iwe, wamphamvu iwe. 13Ndipo
Gideoni ananena naye, Mbuye wanga, ngati Yehova ali nafe
catigwera ife bwanji conseci? ndipo ziti kuti zodabwiza zace zonse
zimene makolo athu anatiwerengera, ndi kuti, Sanatikweza kodi
Yehova kucokera m'Aigupto? Koma tsopano Yehova watitaya
natipereka m'dzanja la Midyani. 14Pamenepo Yehova
anamtembenukira, nati, Muka nayo mphamvu yako iyi,
nupulumutse Israyeli m'dzanja la Midyani, Sindinakutuma ndi Ine
kodi? 15Ndipo anati kwa iye, Ha! Mbuye, ndidzapulumutsa Israyeli
ndi ciani? Taonani, banja langa liri loluluka m'Manase, ndipo ine
ndine wamng'ono m'nyumba ya atate wanga. 16Ndipo Yehova
ananena naye, Popeza Ine ndidzakhala nawe udzakantha Amidyani
ngati munthu mmodzi. 17Ndipo anati kwa iye, Ngati mundikomera
mtima mundionetse cizindikilo tsopano cakuti ndi Inu wakunena
nane. 18Musacoke pano, ndikupemphani, mpaka ndikudzerani ndi

kuturutsa copereka canga ndi kuciika pamaso panu. Ndipo anati, Ndidzalinda mpaka ubwera. 19Ndipo Gideoni analowa, nakonza kambuzi ndi mikate yopanda cotupitsa ya muyeso wa ufa; nyamayi anaiika m'licero, ndi msuzi anauthira mumbale, naturuka nazo kwa iye ali patsinde pa thundu, nazipereka. 20Koma mthenga wa Mulungu ananena naye, Tenga nyamayi ndi mikate yopanda cotupitsa ndi kuziika pathanthwe pano ndi kutsanula msuzi. Ndipo anatero. 21Pamenepo mthenga wa Yehova anatambasula nsonga ya ndodo inali m'dzanja lace, nakhudza nyamayi ndi mikate yopanda cotupitsa; ndipo unaturuka moto m'thanthwe nunyeketsa nyama ndi mikate yopanda cotupitsa; ndi mthenga wa Yehova anakanganuka pamaso pace. 22Pamenepo Gideoni anaona kuti ndiye mthenga wa Yehova, nati Gideoni, Tsoka ine, Yehova Mulungu! popeza ndaona mthenga wa Yehova maso ndi maso. 23Ndipo Yehova anati kwa iye, Mtendere ukhale ndi iwe, usaope, sudzafa. 24Pamenepo Gideoni anammangira Yehova guwa la nsembe pomwepo; nalicha Yehova-ndiyemtendere; likali m'Ofira wa Abieziri ndi pano pomwe.

Gideoni agamula guwa la nsembe la Baala

25Ndipo kunali, usiku womwe uja Yehova ananena naye, Tenga ng'ombe ya atate wako, ndiyo ng'ombe yaciwiri ya zaka zisanu ndi ziwiri, nugamule guwa la nsembe la Baala ndilo la atate wako, nulikhe cifanizo ciri pomwepo; 26numangire Yehova Mulungu wako guwa la nsembe pamwamba pa lingali, monga kuyenera; nutenge ng'ombe yaciwiriyo, nufukize nsembe yopsereza; nkhuni zace uyese cifanizo walikhaco. 27Pamenepo Gideoni anatenga amuna khumi mwa anyamata ace, nacita monga Yehova adanena naye; ndipo kunali, popeza anaopa a ku nyumba ya atate wace, ndi amuna a ku mudziwo, sanacicita msana, koma usiku. 28Ndipo pakuuka mamawa amuna a ku mudziwo, taonani, guwa la nsembe la Baala litagamuka, ndi cifanizo cinali pomwepo citalikhidwa ndi ng'ombe yaciwiri yoperekedwa pa guwa la nsembe adalimanga. 29Nanenana wina ndi mnzace, Wacita ici ndani? Ndipo atafunafuna nafunsafunsa, anati, Gideoni, mwana wa Yoasi wacita ici. 30Pamenepo amuna a ku mudziwo anati kwa Yoasi, Umturutse mwana wako kuti afe; pakuti anagamula guwa la nsembe la Baala, pakutinso analikha cifanizo cinali pomwepo. 31Koma Yoasi anati kwa onse akumuimirira, Kodi inu mumnenera Baala mlandu? Kapena kodi mudzampulumutsa iye? iye amene amnenera mlandu aphedwe kukali m'mawa; akakhala mulungu adzinenere yekha mlandu, popeza wina wamgamulira guwa lace la nsembe. 32Cifukwa cace anamucha tsiku lija Yerubaala, ndi kuti, Amnenece mlandu Baala popeza anamgamulira guwa lace la nsembe.

33Pamenepo Amidyani onse ndi Aamaleki ndi ana a kum'mawa
anasonkhana pamodzi naoloka, namanga misasa m'cigwa ca
Yezreeli. 34Koma mzimu wa Yehova unabvana Gideoni; naomba
lipenga iye, ndi a banja la Abieziri analalikidwa kumtsata
iye. 35Ndipo anatuma mithenga kwa Manase konse; ndi iwonso
analalikidwa kumtsata iye; natuma mithenga kwa Aseri, ndi kwa
Zebuloni, ndi kwa Nafitali; iwo nadzakomana nao. 36Ndipo Gideoni
anati kwa Mulungu, Mukadzapulumutsa Israyeli ndi dzanjalanga
monga mwanena, 37taonani, ndidzaika cikopa ca ubweya
popunthira tirigu; pakakhala mame pacikopa pokha, ndi panthaka
ponse pouma, pamenepo ndidzadziwa kuti mudzapulumutsa
Israyeli ndi dzanja langa monga mwanena. 38Ndipo kunatero;
pakuti anauka mamawa, nafinya cikopaco, nakamula mame a
pacikopa, madzi ace odzala mbale. 39Ndipo Gideoni ananena ndi
Mulungu, Mkwiyo wanu usandiyakire, ndinene kamodzi kokha:
ndikuyeseni kamodzi kokha ndi cikopa; paume pacikopa pokha, ndi
panthaka ponse pakhale mame. 40Ndipo Mulungu anatero usiku
uja; pakuti panauma pacikopa pokha, ndi panthaka ponse panali
mame.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Gideoni apitikitsa nkhondo ya Amidyani

1Pamenepo Yerubaala, ndiye Gideoni, ndi anthu onse okhala naye
anauka mamawa, namanga misasa pa citsime ca Harodi, ndi
misasa ya Midyani inali kumpoto kwao, pa phiri la More
m'cigwa. 2Ndipo Yehova anati kwa Gideoni. Anthu ali ndi iwe
andicurukira kuti ndipereke Midyani m'dzanja lao; angadzitame
Israyeli pa Ine, ndi kuti, Dzanja la ine mwini
landipulumutsa. 3Ndipo tsopano, kalalike m'makutu a anthu, ndi
kuti, Ali yense wocita mantha, nanjenjemera, abwerere nacoke pa
phiri la Gileadi. Ndipo anabwererako anthu zikwi makumi awiri
mphambu ziwiri, natsalako zikwi khumi.
4Ndipo Yehova ananena ndi Gideoni, Anthu akali ocuruka; tsikira
nao kumadzi, ndipo ndidzakuyesera iwo komweko; ndipo kudzali
kuti iye amene ndimnena kwa iwe, Uyo azimuka nawe, yemweyo
azimuka nawe; koma ali yense ndimnena kwa iwe, Uyo asamuke
nawe, yemweyo asamuke. 5Ndipo anatsikira nao anthu kumadzi;
ndipo Yehova anati kwa Gideoni, Ali yense akapiza madzi pa lilime
lace, monga akhatira garu, ameneyo amuike pa yekha; momwemo
ali yense agwada pakumwa. 6Ndi kuwerenga kwa iwo akukhatira,
ndi kuika dzanja lao kukamwa kwao, ndiko mazana atatu; koma
ena onse anagwada pakumwa madzi. 7Ndipo Yehova anati kwa
Gideoni, Ndi anthu mazana atatu akukhatira ndidzakupulumutsani,
ndi kupereka Amidyani m'dzanja lako; koma amuke anthu awa
onse, yense kumalo kwace. 8Pamenepo anthu anatenga kamba
m'dzanja lao, ndi malipenga ao; ndipo anauza amuna onse a
Israyeli amuke, yense kuhema kwace; koma anaimika amuna
mazana atatuwo; ndipo misasa ya Midyani inali kunsi kwace
m'cigwa.
9Ndipo kunali usiku womwewo, kuti Yehova ananena naye, Tauka,
tatsikira kumisasa; pakuti ndaipereka m'dzanja lako. 10Koma ngati
uopa kutsika, utsike naye Pura mnyamata wako
kumisasa; 11nudzamva zonena iwo; utatero manja ako
adzalimbikitsidwa kutsikira kumisasa. Pamenepo anatsikira ndi
Pura mnyamata wace ku cilekezero ca anthu azidaa
m'misasa. 12Ndipo Amidyani ndi Aamaleki ndi ana onse a
kum'mawa ali gonere m'cigwa, kucuruka kwao ngati dzombe; ndi
ngamila zao zosawerengeka, kucuruka kwao ngati mcenga wa
m'mphepete mwa nyanja. 13Ndipo pakufikako Gideoni, taonani,
panali munthu analikufotokozera mnzace loto, nati, Taona, kulota
ndinalota, ndipo tapenya, mtanda wa mkate wabarele
unakunkhulira-kunkhulira m'misasa ya Midyani, nufika kuhema,
numgunda nagwa, numpidigula kuti hema anakhala
cigwere. 14Ndipo mnzace anayankha nati, Ici si cina konse koma

lupanga la Gideoni mwana wa Yoasi, munthu wa Israyeli; Mulungu wapereka Midyani ndi a m'misasa onse m'dzanja lace.
15Ndipo kunali, pakumva Gideoni kufotokozera kwa lotolo ndi tanthauzo lace, anadziwerama; nabwera ku misasa ya Israyeli nati, Taukani, pakuti Yehova wapereka a m'misasa a Midyani m'dzanja lanu. 16Ndipo anagawa amuna mazana atatu akhale magulu atatu, napatsa malipenga m'manja a iwo onse, ndi mbiya zopanda kanthu, ndi miuni m'kati mwa mbiyazo, 17Ndipo ananena nao, Mundipenyerere ine, ndi kucita momwemo; ndipo taonani, pakufika ine pa cilekezero ca misasa, kudzali, monga ndicita ine, momwemo muzicita inu. 18Pamene ndiomba lipenga, ine ndi onse okhala nane, inunso muziomba lipenga pozungulira ponse pa misasa, ndi kunena kuti, Yehova ndi Gideoni.
19Motero Gideoni ndi amuna zana anali naye anafikira ku cilekezero ca misasa poyambira ulonda wa pakati, atasintha alonda tsopano apa; ndipo anaomba malipenga, naphwanya mbiya zokhala m'manja mwao. 20Ndi magulu atatuwo anaomba malipenga, naswa mbiyazo, nagwira miuni ndi dzanja lao lamanzere, ndi malipenga m'dzanja lao lamanja kuwaomba; ndipo anapfuula, Lupanga la Yehova ndi la Gideoni. 21Ndipo anaima yense m'mbuto mwace pozungulira misasa; pamenepo anathamanga a m'misasa onse, napfuula, nathawa. 22Ndipo mazana atatuwa anaomba malipenga, ndipo Yehova anakanthanitsa yense mnzace ndi lupanga m'misasa monse; ndi a m'misasa anathawa mpaka ku Betesita ku Zerera, mpaka ku malire a Abelemehola pa Tabati. 23Pamenepo anthu a Israyeli analalikidwa kucokera ku Nafitali, ndi ku Aseri, ndi ku Manase yense, nalondola Amidyani. 24Gideoni anatumanso mithenga ku mapiri onse a Efraimu ndi kuti, Tsikani, kukomana ndi Amidyani ndi kutsekereza madooko asanafike iwowa, mpaka ku Beti-bara ndi Yordano. Potero amuna onse a Efraimu anasonkhana pamodzi natsekereza madooko mpaka ku Betibara, ndi Yordano. 25Ndipo anagwira akalonga awiri a Midyani, Orebi ndi Zeebi; namupha Orebi ku thanthwe la Orebi; ndi Zeebi anamupha ku coponderamo mphesa ca Zeebi, nalondola Amidyani; ndipo anadza nayo mitu ya Orebi ndi Zeebi kwa Gideoni tsidya lija la Yordano.

©The Bible Society of Malawi, 1992

1Ndipo amuna a Efraimu anati kwa iye, Ici waticitira nciani,
osatiitana popita iwe kulimbana ndi Amidyani? natsutsana naye
kolimba. 2Koma ananena nao, Ndacitanji tsopano monga inu? Kodi
kukunkha mphesa kwa Efraimu sikuposa kuchera mphesa kwa
Abiezeri? 3Mulungu anapereka m'dzanja lanu akalonga a Midyani,
Orebi ndi Zeebi, ndipo ndinakhoza kucitanji monga inu? Pamenepo
mkwiyo wao unamlezera, atanena mau awa.

A ku Sukoti ndi a ku Penueli anyoza Gideoni nalangidwa naye

4Ndipo Gideoni anafika ku Yordano, naoloka, iye ndi amuna
mazana atatu anali naye, ali otopa koma ali cilondolere. 5Ndipo
ananena kwa amuna a ku Sukoti, Mupatsetu anthu awa
akunditsata mitanda yamkate; pakuti atopa, ndipo ndirikulondola
Zeba ndi Tsalimuna mafumu a Midyani. 6Koma akalonga a ku
Sukoti anati, Kodi manja a Zeba ndi Tsalimuna ali m'dzanja lako
tsopano apa, kuti ife tiwaninkhe ankhondo ako mkate? 7Ndipo
Gideoni anati, Cifukwa cace, Yehova akapereka Zeba ndi Tsalimuna
m'dzanja langa, ndidzapuntha nyama yanu ndi minga ya
m'cipululu ndi mitungwi. 8Ndipo anacokapo kukwera ku Penueli,
nanena nao momwemo; ndipo amuna a ku Penueli anamyankha
monga adamyankha amuna a ku Sukoti. 9Ndipo ananenanso kwa
amuna a ku Penueli ndi kuti, Ndikabwerera ndi mtendere
ndidzagumula nsanja iyi.

10Zeba ndi Tsalimuna ndipo anali m'Karikori, ndi a m'misasa ao
pamodzi nao, amuna monga zikwi khumi ndi zisanu; ndiwo otsala
onse a khamu lonse la ana a kum'mawa; popeza atagwa amuna
zikwi zana limodzi ndi makumi awiri akusolola lupanga. 11Ndipo
Gideoni anakwerera njira ya iwo okhala m'mahema kum'mawa kwa
Noba, ndi Yogibea, nakantha khamulo popeza khamulo linakhala
lokhazikika mtima. 12Ndipo Zeba ndi Tsalimuna anathawa; koma
anawatsata, nagwira mafumu awiri a Midyani Zeba ndi Tsalimuna,
nanjenjemeretsa khamu lonse. 13Pamenepo Gideoni mwana wa
Yoasi anabwerera kunkhondo pokwerera pa Heresi. 14Ndipo
anagwira mnyamata wa anthu a ku Sukoti, nafunsira; ndipo
anamsimbira akalonga a ku Sukoti, ndi akulu ace amuna makumi
asanu ndi awiri kudza asanu ndi awiri. 15Ndipo anafika kwa amuna
a ku Sukoti, nati, Tapenyani Zeba ndi Tsalimuna amene
munanditonza nao ndi kuti, Kodi manja a Zeba ndi Tsalimuna
akhala m'dzanja lako, kuti tiwaninkhe mkate amuna ako
akulema? 16Ndipo anagwira akulu, a m'mudzi ndi minga ya
kucipululu ndi mitungwi, nawalanga nazo amuna a ku
Sukoti. 17Ndipo anagamula nsanja ya Penueli, napha amuna a
kumudzi. 18Pamenepo anati kwa Zeba ndi Tsalimuna, Amunawo

munawapha ku Tabori anali otani? Iwo nayankha, Monga iwe momwemo iwowa; yense wakunga mwana wa mfumu. 19Ndipo anati, Ndiwo abale anga, ana a mai wanga. Pali Yehova mukadawasunga amoyo, sindikadakuphani. 20Nati kwa Yeteri mwana wace woyamba, Tauka, nuwaphe. Koma mnyamatayo sanasolola lupanga lace; pakuti anaopa, pokhala anali mnyamata. 21Pamenepo Zeba ndi Tsalimuna anati, Tauka iwe mwini nutigwere; pakuti monga munthu momwemo mphamvu yace. Ndipo Gideoni anauka nawapha Zeba ndi Tsalimuna, nalanda mphande zinali kukhosi kwa ngamila zao.

Gideoni akana kulowa ufumu

22Pamenepo anthu a Israyeli anati kwa Gideoni, Mutilamulire ndi inu, ndi mwana wanu, ndi mdzukulu wanu, pakuti mwatipulumutsa m'dzanja la Amidyani. 23Koma Gideoni ananena nao. Sindidzalamulira inu, ngakhale mwana wanga sadzalamulira inu; Yehova adzalamulira inu. 24Gideoni anatinso kwa iwo, Mundilole ndipemphe kanthu kamodzi kwa inu, mundipatse ali yense mapelele mwa zofunkha zanu; pakuti anali nao mapelele agolidi, pokhala anali Aismayeli. 25Ndipo anayankha, Kupereka tiwapereka; nayalapo cobvala, naponyamo yense mapelele a mwa zofunkha zao. 26Ndipo kulemera kwace kwa mapelele agolidi adawapempha ndiko masekeli cikwi cimodzi ndi mazana asanu ndi awiri; osawerenga mphande, ndi zitunga ndi zobvala zacibakuwa za pa mafumu a ku Midyani, osawerenganso maunyolo okhala pa makosi a ngamila zao. 27Ndipo Gideoni anawapanga fano, naliika m'mudzi mwace, ndiwo Ofira; ndi Israyeli yense analitsata kuligwadira pomwepo; ndipo linakhala kwa Gideoni ndi nyumba yace ngati msampha. 28Motero anagonjetsa Amidyani pamaso pa ana a Israyeli, osaweramutsanso mitu yao iwowa. Ndipo dziko lidapumula zaka makumi anai m'masiku a Gideoni.

29Ndipo Yerubaala, mwana wa Yoasi anamuka, nakhala, m'nyumba ya iye yekha. 30Nakhala nao ana amuna makumi asanu ndi awiri Gideoni, anawabala ndi iye; popeza anali nao akazi ambiri. 31Ndipo mkazi wace wamng'ono wokhala m'Sekemu, iyenso anambalira mwana wamwamuna; namucha dzina lace Abimeleki. 32Ndipo Gideoni mwana wa Yoasi anafa atakalamba bwino, naikidwa m'manda a Yoasi atate wace, m'Ofira wa Aabiezeri.

33Ndipo kunali, atafa Gideoni, ana a Israyeli anabwereranso nagwadira Abaala, nayesa Baala-beriti mulungu wao. 34Ndi ana a Israyeli sanakumbukila Yehova Mulungu wao, amene anawapulumutsa m'dzanja la adani ao onse pozungulira ponse; 35osacitira cifundo nyumba ya Yerubaala, ndiye Gideoni, monga mwa zokoma zonse iye anacitira Israyeli.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Abimeleki awapha abale ace

1Koma Abimeleki mwana wa Yerubaala anamuka ku Sekemu kwa
abale a amai wace, nanena nao, ndi kwa banja lonse la nyumba ya
atate wa amai wace, ndi kuti, 2Nenanitu m'makutu mwa eni ace
onse a ku Sekemu, Cokomera inu nciti, akulamulireni ana amuna
onse a Yerubaala ndiwo amuna makumi asanu ndi awiri, kapena
akulamulireni mwamuna mmodzi? mukumbukilenso kuti ine ndine
wa pfuko lanu ndi nyama yanu. 3Pamenepo abale a amace
anamnenera mau awa onse m'makutu a eni ace onse a Sekemu;
ndi mitima yao inalunjika kutsata Abimeleki; pakuti anati, Ndiye
mbale wathu. 4Ndipo anampatsa ndalama makumi asanu ndi awiri
za m'nyumba ya Baala-beriti; ndipo Abimeleki analembera nazo
anthu opanda pace ndi opepuka amene anamtsata. 5Ndipo
anamuka ku nyumba ya atate wace ku Ofira, nawapha abale ace
ana a Yerubaala, ndiwo amuna makumi asanu ndi awiri, pa
thanthwe limodzi; koma Yotamu mwana wamng'ono wa Yerubaala
anatsalako; pakuti anabisala.
6Pamenepo anasonkhana eni ace onse a ku Sekemu, ndi nyumba
yonse ya Milo, namuka namlonga Abimeleki ufumu pa thundu wa
coimiritsa ciri m'Sekemu.

Fanizo la Yotamu

7Ndipo atamuuza Yotamu, anamuka iye naimirira pamutu pa phiri
la Gerizimu, nakweza mau ace, napfuula, nanena nao, Mundimvere
ine, eni ace a ku Sekemu inu, kuti Mulungu amvere inu. 8Kumuka
inamuka mitengo kudzidzozera mfumu; niti kwa mtengo
waazitona, Ukhale iwe mfumu yathu. 9Koma mtengo waazitona
unati kwa iwo, Ngati ndidzasiya kunona kwanga kumene
alemekeza nako Mulungu ndi anthu kukalenga pa
mitengo? 10Pamenepo mitengo inati kwa mkuyu. Tiye iwe, ukhale
mfumu yathu. 11Koma mkuyu unanena nao, Ngati ndidzasiya
kuzuna kwanga, ndi zipatso zanga zokoma kukalenga pa
mitengo? 12Pamenepo mitengo inati kwa mpesa, Tiye iwe, ukhale
mfumu yathu. 13Koma mpesa unanena nao, Ngati ndidzasiya vinyo
wanga wakusekeretsa Mulungu ndi anthu, kukalenga pa
mitengo? 14Pamenepo mitengo yonse inati kwa nkandankhuku,
Tiye iwe, ukhale mfumu yathu. 15Ndipo nkandankhuku unati kwa
mitengo, Mukandidzoza mfumu yanu moonadi, tiyeni, thawirani ku
mthunzi wanga; mukapanda kutero uturuke mota m'nkandankhuku
ndi kunyeketsa mikungudza ya Lebano. 16Ndipo tsopano, ngati
mwacita moona ndi mwangwiro pakulonga Abimeleki ufumu,
ngatinso mwamcitira cokoma Yerubaala ndi nyumba yace, ndi
kumcitira monga anayenera manja ace; 17pakuti atate wanga
anakugwirirani nkhondo, nataya moyo wace, nakupulumutsani

m'dzanja la Amidyani; 18koma mwaukira nyumba ya atate wanga lero lino, ndi kuwapha ana ace, ndiwo amuna makumi asanu ndi awiri, pa thanthwe limodzi; ndipo mwalonga Abimeleki mwana wa mdzakazi wace, akhale mfumu ya pa eni ace a ku Sekemu, cifukwa ali mbale wanu; 19ngati tsono mwacitira Yerubaala ndi nyumba yace zoona ndi zangwiro lero lino, kondwerani naye Abimeleki, nayenso akondwere nanu; 20koma ngati simunatero, uturuke moto kwa Abimeleki, nunyeketse eni ace a ku Sekemu ndi nyumba ya Milo; nuturuke mota kwa eni ace a ku Sekemu, ndi ku nyumba yace ya Milo, nunyeketse Abimeleki. 21Pamenepo Yotamu anafulumira, nathawa, namuka ku Beeri, nakhala komweko, cifukwa ca Abimeleki mbale wace.

Mpanduko wa Gaala

22Abimeleki atakhala kalonga wa Israyeli zaka zitatu, 23Mulungu anatumiza mzimu woipa pakati pa Abimeleki ndi eni ace a ku Sekemu; ndi eni ace a ku Sekemu anamcitira Abimeleki mosakhulupirika; 24kuti ciwawa adacitira ana amuna makumi asanu ndi awiria Yerubaala cimdzere, ndi kuti mwazi wao uikidwe pa mbale wao Abimeleki anawaphayo, ndi pa eni ace a ku Sekemu, amene analimbikitsa manja ace, awaphe abale ace. 25Ndipo eni ace a ku Sekemu anaika omlalira pamwamba pa mapiri; amene anawawanya onse akudzera njirayi; ndipo anamuuza Abimeleki. 26Ndipo Gaala, mwana wa Ebedi anadza ndi abale ace, napita ku Sekemu; ndi eni ace a ku Sekemu anamkhulupirira. 27Ndipo anaturuka kumka kuminda, nachera mphesa m'mindamo, naponda mphesa, napereka nsembe yolemekeza, nalowa m'nyumba ya mulungu wao, nadya, namwa, natemberera Abimeleki. 28Pamenepo Gaala, mwana wa Ebedi anati, Abimeleki ndani, ndi Sekemu ndani, kuti timtumikire? sindiye mwana wa Yerubaala kodi? ndi Zebuli kazembe wace? Mutumikire amuna a Hamori atate wa Sekemu; koma ameneyo timtumikire cifukwa ninji? 29Mwenzi anthu awa akadakhala m'dzanja langa; ndikadamcotsadi Abimeleki. Ndipo anati kwa Abimeleki, Curukitsa khamu lako, nuturuke. 30Pamene Zebuli woyang'anira mudzi anamva mau a Gaala mwana wa Ebedi, anapsa mtima. 31Natuma mithenga kwa Abimeleki monyenga nati, Taonani Gaala ndi abale ace afika ku Sekemu; ndipo taonani, akupandukitsirani mudzi. 32Ndipo tsopano, taukani usiku, inu ndi anthu okhala nanu ndi kulalira kuthengo; 33ndipo kukhale kuti m'mawa, pakuturuka dzuwa, muuke mamawa mugwere mudziwo; ndipo taonani, akakuturukirani iye ndi anthu ali naye, uzimcitira monga lidziwa dzanja lako.

34Pamenepo Abimeleki anauka ndi anthu onse anali naye, usiku; nalalira a ku Sekemu, magulu anai. 35Ndipo Gaala mwana wa Ebedi

anaturuka, naima polowera pa cipata ca mudzi; nauka Abimeleki ndi anthu anali naye m'molalira. 36Ndipo pamene Gaala anapenya anthuwo anati kwa Zebuli, Taona, alikutsika anthu kucokera pamwamba pa mapiri, Koma Zebuli ananena naye, Uona mthunzi wa mapiri ndi kuyesa anthu. 37Koma Gaala ananenanso, nati, Tapenya alikutsika anthu pakati pa dziko, ndi gulu limodzi lidzera olira ya ku thundu wa alauli. 38Pamenepo Zebuli anati kwa iye, Pakamwa pako mpoti tsopano, muja udanena, Ndani Abimeleki kud timtumikire? awa si anthuwo unawapeputsa? uturuke tsopano, nulimbane nao. 39Ndipo Gaala anaturuka pamaso pao pa eni ace a ku Sekemu, nalimbana ndi Abimeleki. 40Koma Abimeleki anampitikitsa, nathawa iye pamaso pace; nagwa olasidwa ambiri mpaka polowera pa cipata. 41Ndipo Abimeleki anakhala ku Aruma; ndi Zebuli anafngitsa Gaala ndi abale ace kuti asakhale m'Sekemu. 42Ndipo kunali m'mawa mwace, kuti anthu anaturuka kumka kuminda; ndipo anauza Abimeleki. 43Pamenepo anatenga anthu, nawagawa magulu atatu, nalalira m'minda; napenya, ndipo taonani, anthu alimkuturuka m'mudzi; nawaukira iye nawakantha. 44Ndi Abimeleki ndi magulu okhala naye anathamanga naima polowera pa cipata ca mudzi; ndi magulu awiriwo anagwera onse okhala m'munda, nawakantha. 45Ndipo Abimeleki analimbana ndi mudzi tsiku lija lonse; nalanda mudzi nawapha anthu anali m'mwemo; napasula mudzi; nawazapo mcere.
46Ndipo pamene eni ace onse a nsanja ya ku Sekemu anacimva, analowa m'ngaka ya nyumba ya Eliberiti. 47Ndipo anauza Abimeleki kuti amuna onse a nsanja ya ku Sekemu asonkhane. 48Pamenepo Abimeleki anakwera kumka ku phiri la Zalimoni, iye ndi anthu onse anali naye; natenga nkhwangwa m'dzanja lace Abimeleki, nadula nthambi kumitengo, nainyamula ndi kulika paphewa pace, nati kwa anthu okhala naye, Ici munaciona ndacita, fulumirani, mucite momwemo. 49Ndi anthu onse anadulanso yense nthambi yace, natsata Abimeleki, naziika pangaka, natentha nazo ngakayo ndi moto; motero anthu onse a nsanja ya ku Sekemu anafanso, amuna ndi akazi ngati cikwi cimodzi.

Imfa ya Abimeleki

50Pamenepo Abimeleki anamuka ku Tebetsi, naumangira Tebetsi misasa, naulanda. 51Koma m'mudzimo munali nsanja yolimba nathawira kumeneko amuna ndi akazi onse, ndi eni ace onse a mudziwo, nadzitsekereza m'mwemo, nakwera patsindwi pa nsanja. 52Ndipo Abimeleki anafika kunsania, nalimbana nayo nkhondo, nayandikira kukhomo kwa nsanja, aitenthe ndi moto. 53Ndipo mkazi wina anaponya mwana wa mphero pamutu

pa Abimeleki, naphwanya bade lace. 54Pamenepo anaitana msanga mnyamata wace wosenza zida zace, nanena naye, Solola lupanga lako nundiphe, angamanenere anthu, ndi kuti, Anamupha ndi mkazi. Nampyoza mnyamata wace, nafa iye. 55Pamene amuna a Israyeli anaona kuti adafa Abimeleki anamuka yense kumalo kwace. 56Momwemo Mulungu anambwezera Abimeleki coipaco anacitira atate wace ndi kuwapha abale ace makumi asanu ndi awiri. 57Ndipo Mulungu anawabwezera coipa conse ca amuna a ku Sekemu pamitu pao, ndipo linawagwera temberero la Yotamu mwana wa Yerubaala.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Tola ndi Yairi aweruza Israyeli

1Atafa Abimeleki, anauka kupulumutsa Israyeli Tola mwana wa
Puwa, mwana wa Dodo munthu wa Isakara; nakhala iye m'Sanriri
ku mapiri a Efraimu. 2Ndipo anaweruza Israyeli zaka makumi awiri
ndi zitatu, nafa, naikidwa m'Samiri.
3Atafa iye, anauka Yairi Mgileadi, naweruza Israyeli zaka makumi
awiri mphambu ziwiri. 4Ndipo anali nao ana amuna makumi atatu
okwera pa ana a aburu makumi atatu, iwo ndipo anali nayo midzi
makumi atatu, ochedwa midzi ya Yairi, mpaka lero lino, ndiyo
m'dziko la Gileadi. 5Nafa Yairi, naikidwa m'Kamoni.

Aisrayeli acimwira Mulungu nagonjetsedwa ndi Afilisti ndi Amoni

6Ndipo ana Israyeli a anaonjeza kucita coipa pamaso pa Yehova,
natumikira Abaala, ndi Aastaroti, ndi milungu ya Aramu, ndi
milungu ya Sidoni, ndi milungu ya Moabu, ndi milungu ya ana a
Amoni, ndi milungu ya Afilisti; ndipo anamleka Yehova
osamtumikira. 7Pamenepo mkwiyo wa Yehova unayakira Israyeli,
nawagulitsa m'dzanja la Aftlisti, ndi m'dzanja la ana a
Amoni. 8Ndipo anaphwanya napsinja ana a Israyeli caka ciija,
natero ndi ana onse a Israyeli okhala tsidya lija la Yordano m'dziko
la Aamori, ndilo Gileadi, zaka khumi ndi zisanu ndi zitatu. 9Ndipo
ana a Amoni anaoloka Yordano kuthiranso nkhondo Yuda ndi
Benjamini, ndi nyumba ya Efraimu; napsinjika kwambiri
Israyeli. 10Ndipo ana a Israyeli anapfuula kwa Yehova ndi kuti,
Takucimwirani, popeza tasiya Mulungu wathu ndi kutumikira
Abaala. 11Ndipo Yehova anati kwa ana a Israyeli, Kodi
sindinakupulumutsani kwa Aaigupto ndi kwa Aamori, ndi kwa ana a
Amoni, ndi kwa Aftlisti? 12Asidoni omwe, ndi Aamaleki, ndi
Amidyani anakupsinjani. Pamenepo munapfuula kwa Ine, ndipo
ndinakupulumutsani m'dzanja lao. 13Koma mwandisiya Ine ndi
kutumikira milungu yina, cifukwa cace
sindikupulumutsaninso. 14Mukani ndi kupfuulira kwa milungu
munaisankha, ikupulumutseni nyengo ya kusauka kwanu. 15Koma
ana a Israyeli anati kwa Yehova, Tacimwa, muticitire monga mwa
zonse zikomera pamaso panu; komatu mutipulumutse lero lino,
tikupemphani. 16Pamenepo anacotsa milungu yacilendo pakati
pao, natumikira Yehova; ndipo mtima wace unagwidwa cisoni
cifukwa ca mabvuto a Israyeli.
17Ndipo ana a Amoni analalikiridwa, namanga misasa m'Gileadi.
Ndi ana a Israyeli anasonkhana namanga misasa ku
Mizipa. 18Ndipo anthu, akalonga a Gileadi, ananenana wina ndi
mnzace, Ndaniyo adzayamba kulimbana ndi ana a Amoni? iye
adzakhala mkuru wa onse okhala m'Gileadi.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Yefita alanditsa Israyeli

1Yefita Mgileadi ndipo anali ngwazi yamphamvu, ndiye mwana wa
mkazi wadama; koma Gileadi adabala Yefita. 2Ndipo mkazi wa
Gileadi anambalira ana amuna; koma atakula ana amuna a
mkaziyo anampitikitsa Yefita, nanena naye, Sudzalandira colowa
m'nyumba ya atate wako; pakuti ndiwe mwana wa mkazi
wina. 3Pamenepo Yefita anathawa abale ace, nakhala m'dziko la
Tobu; ndipo anyamata opanda pace anasonkhana kwa Yefita,
naturuka naye pamodzi.
4Ndipo kunali, atapita masiku, ana a Amoni anacita nkhondo ndi
Israyeli, 5ndipo kunatero, pamene ana a Amoni anathira nkhondo
pa Israyeli, akuru a Gileadi anamuka kutenga Yefita m'dziko la
Tobu; 6nati kwa Yefita, Tiye ukhale kazembe wathu kuti tilimbane
ndi ana a Amoni. 7Ndipo Yefita anati kwa akulu a Gileadi,
Simunandida kodi, ndi kundicotsa m'nyumba ya atate wanga?
ndipo mundidzeraoji tsopano pokhala muli m'kusauka? 8Ndipo
akuru a Gileadi ananena ndi Yefita, Cifukwa cace cakuti
takubwerera tsopano ndico kuti umuke nafe ndi kucita nkhondo ndi
ana a Amoni, nudzakhala mkuru wathu wa pa onse okhala
m'Gileadi. 9Ndipo Yefita anati kwa akuru a Gileadi,
Mukaodifikitsanso kwathu kucita nkhondo ndi ana a Amoni,
nakawapereka Yehova pamaso panga, ndidzakhala mkuru wanu
kodi? 10Ndipo akuru a Gileadi anati kwa Yefita, Yehova ndiye
wakumvera pakati pa ife, tikapanda kucita monga momwe
wanena. 11Pamenepo Yefita anamuka ndi akuru a Gileadi, ndipo
anthu anamuika mkuru wao ndi mtsogoleri wao; ndipo Yefita
ananena mau ace onse pamaso pa Yehova ku Mizipa.
12Ndipo Yefita anatuma mithenga kwa mfumu ya ana a Amoni, ndi
kuti, Ndi ciani ndi Inu, ndi kuti Mwandidzera kuthira nkhondo dziko
langa? 13Ndipo mfumu ya ana a Amoni inati kwa mithenga ya
Yefita, Cifukwa Israyeli analanda dziko langa pakukwera iye
kucokera ku Aigupto, kuyambira Arinoni mpaka Yaboki, ndi mpaka
Yordano; ndipo tsopano uodibwezere maikowa
mwamtendere. 14Ndipo Yefita anatumanso mithenga kwa mfumu
ya ana a Amoni; 15nanena naye, Atero Yefita, Israyeli sanalanda
dziko la Moabu kapena dziko la ana a Amoni; 16pakuti pakukwera
iwo kucokera ku Aigupto Israyeli anayenda m'cipululu mpaka
Nyanja Yofiira, nafika ku Kadesi; 17pamenepo Israyeli anatuma
mithenga kwa mfumu ya Edomu, ndi kuti, Ndikupemphani ndipitire
pakati pa dziko lanu; koma mfumu ya Edomu sinamvera.
Natumanso kwa mfumu ya Moabu; nayenso osalola; ndipo Israyeli
anakhala m'Kadesi. 18Pamenepo anayenda m'cipululu, naphazira
dziko la Edomu, ndi dziko la Moabu, nadzera kum'mawa kwa dziko

la Moabu, namanga misasa tsidya lija la Arinoni; osalowa malire a Moabu, pakuti Arinoni ndi malire a Moabu. 19Ndipo Israyeli anatuma mithenga kwa Sihoni mfumu ya Aamori, mfumu ya ku Hesiboni; nanena naye Israyeli, Tikupemphani tipitire pakati pa dziko lanu, kumka kwathu. 20Koma Sihoni sanakhulupirira Israyeli kuti apitire pakati pa malire ace; koma Sihoni anamemeza anthu ace onse, namanga misasa ku Yahazi, nathira nkhondo Israyeli. 21Ndipo Yehova Mulungu wa Israyeli anapereka Sihoni ndi anthu ace onse m'dzanja la Israyeli, ndipo anawakantha, ndi Israyeli analandira colowa cace, dziko lonse la Aamori, nzika za m'dziko lija. 22Ndipo analandira akhale colowa cao, malire onse a Aamori, kuyambira Arihoni mpaka Yaboki, ndi kuyambira cipululu mpaka Yordano. 23Motero Yehova Mulungu wa Israyeli anaingitsa Aamori, pamaso pa anthu ace Israyeli, ndipo kodi liyenera kukhala colowa canu? 24Cimene akulandiritsani Kemosi mulungu wanu, simucilandira colowa canu kodi? Momwemo ali yense Yehova Mulungu wathu waiogitsa pamaso pathu, zacezo tilandira colowa cathu. 25Ndipo tsopano kodi inu ndinu wabwino woposa Balaki mwana wa Zipori, mfumu ya Moabu; anatengana konse ndi Israyeli iyeyu kodi, kapena kucita nao nkhondo konse kodi? 26Pokhala Israyeli m'Hesiboni ndi midzi yace, ndi m'Aroeri ndi midzi yace, ndi m'midzi yonse yokhala m'mphepete mwa Arinoni zaka mazana atatu; munalekeranji kulandanso nthawi ija? 27Potero sindinakucimwirani ine, koma mundicitira coipa ndinu kundithira nkhondo; Yehova, Woweruzayo, aweruze lero lino pakati pa ana a Israyeli ndi ana a Amoni. 28Koma mfumu ya ana a Amoni sanamvera mau a Yefita anamtumizirawo.

Cowinda ca Yefita

29Pamenepo mzimu wa Yehova unamdzera Yefita, napitira iye ku Gileadi, ndi Manase, napitira ku Mizipa wa Gileadi, ndi kucokera ku Mizipa wa Gileadi anapitira kwa ana a Amoni. 30Ndipo Yefita anawindira Yehova cowinda, nati, Mukaperekatu ana a Amoni m'dzanja langa, ndipo kudzali kuti ciri conse cakuturuka pakhomo pa nyumba yanga kudzakomana nane pakubweranso ine ndi mtendere kucokera kwa ana a Amoni, cidzakhala ca Yehova, ndipo ndidzacipereka nsembe yopsereza. 32Potero Yefita anapita kwa ana a Amoni kuwathira nkhondo; ndipo Yehova anawapereka m'dzanja lace; 33nawakantha kuyambira ku Aroeri mpaka ufika ku Miniti, ndiyo midzi makumi awiri, ndi ku Abelikerami, makanthidwe akuru ndithu. Motero ana a Amoni anagonjetsedwa pamaso pa ana a Israyeli.

34Pofika Yefita ku Mizipa ku nyumba yace, taonani, mwana wace wamkazi anaturuka kudzakomana naye ndi malingaka ndi kuthira mang'ombe; ndipo iyeyu anali mwana wace mmodzi yekha,

analibe mwana wina wamwamuna kapena wamkazi. 35Ndipo kunali, pakumuona anang'amba zobvala zace, nati, Tsoka ine, mwana wanga, wandiweramitsa kwakukuru, ndiwe wa iwo akundisaukitsa ine; pakuti ndamtsegulira Yehova pakamwa panga ine, ndipo sinditha kubwerera. 36Ndipo anati kwa iye, Atate wanga, mwamtsegulira Yehova pakamwa panu, mundicitire ine monga umo mudaturutsa mau pakamwa panu; popeza Yehova anakucitirani inu cilango pa adani anu, pa ana a Amoni. 37Ndipo anati kwa atate wace, Andicitire ici, andileke miyezi iwiri, kuti ndicoke ndi kutsikira kumapiri, ndi kulirira unamwali wanga, ine ndi anzanga. 38Nati iye, Muka. Namuuza amuke akakhale miyezi iwiri; namuka iye ndi anzace, nalirira unamwali wace pamapiri. 39Ndipo kunali pakutha miyezi iwiri, anabwerera kwa atate wace amene anamcitira monga mwa cowinda cace anaciwinda; ndipo sanamdziwa mwamuna. Motero unali mwambo m'Israyeli, 40kuti ana akazi a Israyeli akamuka caka ndi caka kumliriririra mwana wa Yefita wa ku Gileadi, masiku anai pa caka.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Efraimu aukira Yefita

1Pamenepo amuna a Efraimu analalikidwa, napita kumpoto; nati
kwa Yefita, Wapitiriraoji kuthira nkhondo ana a Amoni, osatiitana
ife timuke nawe? Tidzakutenthera nyumba yako
ndimotopamtupako. 2Ndipo Yefita anati kwa iwo, Ine ndi anthu
anga tinatsutsana kwakukuru ndi ana a Amoni, koma pamene
ndinakuitanani inu simunandipulumutsa m'dzanju lao. 3Ndipo
pakuona ine kuti simunandipulumutsa, ndinataya moyo wanga ndi
kupita kwa ana a Amoni; ndipo Yehova anawapereka m'dzanja
langa; mwakwereranji tsono lero lino kundicitira
nkhondo? 4Pamenepo Yefita anamemeza amuna onse a m'Gileadi
nalimbana naye Efraimu; ndipo amuna a Gileadi anakantha
Efraimu, cifukwa adati, Inu Agileadi ndinu akuthawa Efraimu,
pakati pa Efraimu ndi pakati pa Manase. 5Ndipo Agileadi
anatsekereza madooko a Yordano a Efraimu; ndipo kunatero kuti,
akati othawa a Efraimu, Ndioloke, amuna a Gileadi anati kwa iye,
Ndiwe M-efraimu kodi? Akati, Iai; 6pamenepo anati kwa iye, Unene
tsono Shiboleti; ndipo akati, Siboleti, osakhoza kuchula bwino,
amgwira namupha padooko pomwe pa Yordano; ndipo anagwa a
Efraimu nthawi ija, zikwi makumi anai mphambu ziwiri.
7Ndipo Yefita anaweruza Israyeli zaka zisanu ndi cimodzi; nafa
Yefita Mgileadi, naikidwa m'mudzi wina wa Gileadi.

Oweruza Ibzani, Eloni, Abidoni

8Ndi pambuyo pace Ibzani wa ku Betelehemu anaweruza
Israyeli. 9Ndipo anali nao ana amuna makumi atatu; ndi ana akazi
makumi atatu anawakwatitsa kwina, natengera ana ace amuna
ana akazi makumi atatu ocokera kwina. Ndipo anaweruza Israyeli
zaka zisanu ndi ziwiri. 10Nafa Ibzani naikidwa ku Betelehemu.
11Ndi pambuyo pace Eloni Mzebuloni anaweruza Israyeli; naweruza
Israyeli zaka khumi. 12Nafa Eloni Mzebuloni naikidwa m'Aijaloni
m'dziko la Zebuloni.
13Ndi pambuyo pace Abidonf mwana wa Hilele wa ku Piratoni
anaweruza Israyeli. 14Ndipo anali nao ana amuna makumi anai ndi
zidzukulu zazimuna makumi atatu, akuyenda okwera pa ana a
aburu makumi asanu ndi awiri; naweruza Israyeli zaka zisanu ndi
zitatu. 15Nafa Abidoni mwana wa Hilele wa ku Piratoni, naikidwa
m'Piratoni m'dziko la Efraimu ku mapiri a Amaleki.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Oweruza 13

Aisrayeli agonjera Afilisti; abadwa Samsoni

1Ndipo ana a Israyeli anaonjeza kucita coipa pamaso pa Yehova;
nawapereka Yehova m'dzanja la Afilisti zaka makumi anai.
2Ndipo panali munthu wina wa Zora wa banja la Adani, dzina lace
ndiye Manowa; ndi mkazi wace analibe mwana, sanabala. 3Ndipo
mthenga wa Yehova anamuonekera mkaziyo nanena naye, Taona
tsopano, ulibe mwana, wosabala iwe; koma udzaima ndi kubala
mwana wamwamuna. 4Cifukwa cace udzisamalire, usamwe vinyo
kapena coledzeretsa, nusadye cinthu ciri conse codetsa; 5pakuti
taona, udzaima, nudzabala mwana wamwamuna; pamutu pace
sipadzafika lumo; pakuti mwanayo adzakhalira kwa Mulungu
Mnaziri cibadwire; nadzayamba iye kupulumutsa Israyeli m'dzanja
la Afilisti. 6Pamenepo anadza mkaziyo, nanena ndi mwamuna wace
ndi kuti, Wandidzera munthu wa Mulungu; maonekedwe ace ndiwo
ngati maonekedwe a mthenga wa Mulungu oopsa ndithu; ndipo
sindinamfunsa uko acokera kapena sanandiuzanso dzina
lace; 7koma anati kwa ine, Taona, udzaima, ndi kubala mwana
wamwamuna; ndipo tsopano usamwe vinyo kapena coledzeretsa,
nusadye ciri conse codetsa; pakuti mwanayo adzakhalira kwa
Mulungu Mnaziri cibadwire mpaka tsiku la kufa kwace. 8Pamenepo
Manowa anapembedza Yehova, nati, Yehova, ndikupemphani,
atidzerenso munthu wa Mulungu mudamtumayo, natilangize ico
tizicitira mwanayo akadzabadwa. 9Ndipo Mulungu anamvera mau a
Manowa; ndi mthenga wa Mulungu anamdzeranso mkaziyo,
pamene anali m'munda, mwanuna wace Manowa palibe. 10Ndipo
mkaziyo anafulumira nathamanga, nauza mwamuna wace, nanena
naye, Taona, wandionekera munthu anandidzerayo tsiku
lija. 11Nanyamuka Manowa natsata mkazi wace, namdzera
mwamuna uja, nanena naye, Kodi ndinu mwamuna
ujamunalankhulandimkaziyu? Ndipo anati, Ndine amene. 12Nati
Manowa, Acitike tsopano mau anu; koma makhalidwe ace a
mwanayo ndi macitidwe ace adzatani? 13Ndipo mthenga wa
Yehova anati kwa Manowa, Zonse ndinazinena ndi mkazi
azisamalire. 14Ciri conse cicokera kumpesa asadyeko, asamwe
vinyo kapena coledzeretsa, kapena kudya ciri conse codetsa;
zonse ndinamlamulira azisunge. 15Ndipo Manowa anati kwa
mthenga wa Yehova, Tiloleni tikucedwetseni kuti tikukonzereni
mwana wa mbuzi. 16Koma mthenga wa Yehova anati kwa Manowa,
Ungakhale undicedwetsa, sindidzadya mkate wako; ndipo
ukakonza nsembe yopsereza, uziipereka kwa Yehova. Pakuti
Manowa sanadziwa kuti ndiye mthenga wa Yehova. 17Ndipo
Manowa anati kwa mthenga wa Yehova, Dzina lanu ndani, kuti,
atacitika mau anu, tikucitireni ulemu. 18Ndipo mthenga wa Yehova

anati kwa iye, Ufunsiranji dzina langa, popeza liri lodabwitsa? 19Pamenepo Manowa anatenga mwana wa mbuzi pamodzi ndi nsembe yaufa, nazipereka kwa Yehova pathanthwe; ndipo mthengayo anacita modabwitsa, ndi Manowa ndi mkazi wace ali cipenyereo 20Pakuti kunali, pakukwera lawi la mota pa guwa la nsembe kumwamba, mthenga wa Yehova anakwera m'lawi la pa guwalo; ndi Manowa ndi mkazi wace ali cipenyere; nagwa iwowa nkhope zao pansi. 21Ndipo mthenga wa Yehova sanaonekeranso kwa Manowa kapena kwa mkazi wace. Pamenepo anadziwa Manowa kuti ndiye mthenga wa Yehova. 22Nati Manowa kwa mkazi wace, Tidzafa ndithu pakuti taona Mulungu. 23Koma mkazi wace ananena naye, Yehova akadafuna kutipha, sakadalandira nsembe yopsereza ndi nsembe yaufa pa dzanja lathu, kapena kutionetsa izi zonse, kapena kutimvetsa zoterezi nthawi yino. 24Ndipo mkaziyo anabala mwana wamwamuna namucha dzina lace Samsoni; nakula mwanayo, Yehova namdalitsa. 25Ndipo mzimu wa Yehova unayamba kumfulumiza mtima ku misasa ya Dani pakati pa Zora ndi Esitaoli.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Ukwati wa Samsoni

1Ndipo Samsoni anatsikira ku Timna, naona mkazi wa ku Timna wa
ana akazi a Afilisti. 2Nakwera iye, nauzaatatewacendi amai wace,
nati, Ndapenya mkazi m'Timna wa ana akazi a Afilisti; ndipo tsono
munditengere uyu akhale mkazi wanga. 3Koma atate wace ndi
amai wace ananena naye, Kodi palibe mkazi mwa ana akazi a
abale ako, kapena mwa anthu a mtundu wanga onse, kuti wamuka
kutenga mkazi wa Afilisti osadulidwawo? Nati Samsoni kwa atate
wace, Nditengereni iye, pakuti andikonda pamaso panga. 4Koma
atate wace ndi amai wace sanadziwa kuti cidacokera kwa Yehova
ici; popeza analikufuna kutola cifukwa ndi Afilisti. Ndipo nthawi ija
Afilisti analamulira Israyeli.

Samsoni apha mkango

5Pamenepo anatsikira Samsoni, ndi atate wace ndi mai wace ku
Timna, nadza ku minda yamphesa ya Timna; ndipo taona, mwana
wa mkango wakomana naye namdzumira. 6Ndipo unamgwera iye
kolimba mzimu wa Yehova, naung'amba monga akadang'amba
mwana wa mbuzi, wopandakanthu m'dzanjaliace; koma sanauza
atate wace kapena amai wace cimene adacicita. 7Ndipo anatsika
nakamba ndi mkazi, namkonda Samsoni pamaso pace. 8Atapita
masiku ndipo anabweranso kudzamtenga, napambuka iye kukaona
mtembo wa mkango; ndipo taona, m'citanda ca mkango munali
njuci zoundana, ndi uci. 9Ndipo anaufula ndi dzanja lace, nayenda,
namadya alimkuyenda, nadza kwa atate wace ndi amai wace,
nawapatsa, nadya iwo; koma sanawauza kuti adaufula uciwo
m'citanda ca mkango.

Awaphera anthu mwambi

10Ndipo atate wace anatsikira kwa mkazi; ndi Samsoni
anakonzerapo madyerero; pakuti amatero anyamata. 11Ndipo
kunali, pamene anamuona, anabwera nao anzace makumi atatu
akhale naye. 12Nanena nao Samsoni, Mundilole ndikuphereni
mwambi; mukanditanthauziratu uwu m'masiku asanuwa a
madyerero, ndi kuukumika uwu, ndidzakupatsani malaya a nsaru
yabafuta makumi atatu, ndi zobvala zosinthanitsa makumi
atatu; 13koma ngati simukhoza kunditanthauzira uwu
mudzandipatsa ndinu Malaya a nsaru yabafuta makumi atatu ndi
zobvala zosinthanitsa makumi atatu. Pamenepo ananena naye,
Mwambi wako tiumve. 14Ndipo ananena nao,

Cakudya cinaturuka m'mwini kudya,
Ndi cozuna cinaturuka m'mwini mphamvu,

Ndipo masiku atatu sanakhoza kutanthauzira mwambiwo. 15Koma
kunali, tsiku lacisanu ndi ciwiri anati kwa mkazi wa Samsoni, Kopa
mwamuna wako, atitanthauzire mwambiwo; tingatenthe iwe ndi

nyumba ya atate wako ndi mota. Kodi mwatiitana kulanda zathu; si momwemo? 16Ndipo mkazi wa Samsoni analira pamaso pace, nati, Ungondida, osandikonda; waphera anthu a mtundu wanga mwambi, osanditanthauzira ine. Ndipo ananena naye, Taona, sindinatanthauzira atate wanga kapena amai wanga, kodi ndikutanthauzire iwe? 17Ndipo analira pamaso pace masiku asanu ndi awiriwo pocitika madyerero ao; koma kunali kuti tsiku lacisanu ndi ciwiri anamuuza, popeza anamuumiriza; ndipo anatanthauzira anthu a mtundu wace mwambiwo. 18Ndipo amuna a pamudzi anati kwa Samsoni tsiku lacisanu ndi ciwiri, lisanalowe dzuwa, Cozuna coposa uci nciani; ndi camphamvu coposa mkango nciani?
Pamenepo ananena nao,
Mukadapanda kulima ndimthandi wanga,
Simukadakumika mwambi wanga.
19Ndipo mzimu wa Yehova unamgwera Samsoni, natsikira iye kwa Asikeloni, nawakantha amuna makumi atatu, natenga zobvala zao, nawapatsa okumika mwambiwo zobvala zosinthanitsa. Koma adapsa mtima, nakwera kumka ku nyumba ya atate wace. 20Ndipo mkazi wace wa Samsoni anakhala wa mnzace, amene adakhala bwenzi lace.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Samsoni atentha za m'minda ya Afilisti

1Ndipo kunali atapita masiku, nyengo ya kuceka tirigu Samsoni
anakaceza ndi mkazi wace ndi kumtengera mbuzi, nati,
Ndidzalowa kwa mkazi wanga kucipinda. Koma atate wace
sanamlola kulowamo. 2Nati atate wace, Ndinanenetsa kuti umuda
konse, potero ndinampereka kwa bwenzi tako; mng'ono wace
sakoma koposa iye nanga? ukhale naye, m'malo mwa
winayu. 3Koma Samsoni ananena nao, Nthawi yino ndikhala
wosaparamula pa Afilisti, powacitira coipa ine. 4Namuka Samsoni,
nagwira ankhandwe mazana atatu, natenga miuni, nalunza micira,
naika muuni pakati pa micira iwiri iri yonse. 5Nayatsa miuni,
nawataya ku tirigu wosaceka wa Afilisti, natentha miulu ndi tirigu
wosaceka yemwe, ndi minda ya azitona yomwe. 6Pamenepo Afilisti
anati, Wacita ici ndani? Nati, Samsoni mkamwini wa munthuyo wa
ku Timna, popeza analanda mkazi wace, nampereka kwa mnzace.
Pamenepo Afilisti anakwera namtentha mkaziyo ndi atate wace ndi
moto. 7Ndipo Samsoni ananena nao, Mukatero ndidzakubwezerani
cilango ndi pamenepo ndidzaleka. 8Ndipo anawakantha
nyung'unyu ndi ncafu, makanthidwe akuru; natsika nakhala
m'phanga mwa thanthwe la ku Etamu.

Ayesa kumanga Samsoni, napha ive anthu ambiri

9Pamenepo Afilisti anakwera, namanga misasa m'Yuda, natandika
m'Leki 10Ndipo anthu a Yuda anati, Mwatikwerera cifukwa ninji?
Nati iwo, Takwera kumanga Samsoni, kumcitira iye monga
anaticitira ife. 11Pamenepo anatsikira ku phanga la Etamu amuna
zikwi zitatu, nati kwa Samsoni, Sudziwa kodi kuti Atilisti ndiwo
akutilamulira ife? nciani ici waticitira? Nati iye kwa iwowa, Monga
anandicitira ine ndawacitira iwo. 12Ndipo ananena naye, Tatsika ife
tikumange, kuti tikupereke m'dzanja la Atilisti. Nanena nao
Samsoni, Mundilumbirire kuti simudzandigwera nokha. 13Ndipo
anati kwa iye, Iai, koma kumanga tidzakumanga, ndi kukupereka
m'dzanja lao; koma kupha sitikupha iwe. Nammanga iye ndi
zingwe ziwiri zatsopano, nakwera naye kucokera
kuthanthwe. 14Pamene anafika ku Leki Afilisti anapfuula pokomana
naye; koma mzimu wa Yehova unamgwera kolimba, ndi zingwe
zokhala pa manja ace zinanga bwazi lopserera ndi moto, ndi
zomangira zace zinanyotsoka pa manja ace. 15Ndipo anapeza
cibwano catsopano ca buru, natambasula dzanja lace nacigwira,
nakantha naco amuna cikwi cimodzi. 16Nati Samsoni,

Ndi cibwano ca buru, miuru miuru,
Amuna cikwi ndawakantha ndi cibwano ca buru.

17Ndipo kunali, atatha kunena, anataya cibwano m'dzanja lace;
nawacha maiowo Ramati-leki ndiko kunena citunda ca

cibwano. 18Ndipo anamva ludzu lambiri, naitana kwa Yehova, nati,
Mwapatsa Inu cipulumutso ici cacikuru ndi dzanja la kapolo wanu;
ndipo kodi ndife nalo ludzu tsopano ndi kugwa m'dzanja la
osadulidwa awa? 19Pamenepo Mulungu anang'amba pokumbika
paja pit Leki, naturukamo madzi; namwa iye, nubwera moyo wace,
natsitsimuka iye; cifukwa cace anawacha dzina lace, Kasupe wa
wopfuula, ndiwo m'Leki mpaka lero lino. 20Ndipo Samsoni
anaweruza Israyeli m'masiku a Afilisti zaka makumi awiri.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Oweruza 16

Delila apereka Samsoni

1Ndipo Samsoni anamuka ku Gaza, naonako mkazi wadama,
nalowana naye. 2Koma wina anauza a ku Gala, ndi kuti, Samsoni
walowa kuno. Pamenepo anamzinga, namlalira usiku wonse pa
cipata ca mudzi, nakhala cete usiku wonse ndi kuti, Tidikire mpaka
kuca, pamenepo tidzamupha, 3Koma Samsoni anagona mpaka
pakati pa usiku, nauka pakati pa usiku, nagwira zitseko za pa
cipata ca mudzi, ndi mphuthu ziwirizo, nazicotsa ndi mpiringidzo
womwe, naziika pa mapewa ace, nakwera nazo pamwamba pa
phiri liri pandunji pa Hebroni.
4Ndipo pambuyo pace kunali kud anakonda mkazi m'cigwa ca
Soreki, dzina lace ndiye Delila. 5Ndipo akalonga a Atilisti
anamkwerera mkaziyo, nanena naye, Umkope nuone umo
mucokera mphamvu yace yaikuru, ndi umo tingakhoze kumtha
khama, kuti timmange kumzunza; ndipo tidzakupatsa ali yense
ndalama mazana khumi ndi limodzi. 6Pamenepo Delila anati kwa
Samsoni, Ndikupempha, undiuze umo mucokera mphamvu yako
yaikuru, ndi cimene angakumange naco, kuti akuzunze. 7Nanena
naye Samsoni, Akandimanga nazo nsinga zatsopano zisanu ndi
ziwiri zosauma, ndidzakhala wofoka, wakunga munthu
wina. 8Pamenepo akalonga a Afilisti anakwera nazo kwa mkaziyo
nsinga zatsopano zisanu ndi ziwiri zosauma; ndipo iye anammanga
nazo. 9Koma anali nao omlalira m'cipinda ca m'kati. Nanena naye,
Afilisti akugwera, Samsoni, Pamenepo anadula nsingazi, monga
iduka nkhosi ya bwazi pokhudza moto. M'mwemo mphamvu yace
siinadziwike. 10Pamenepo Delila anati kwa Samsoni, Taona,
wandipusitsa, ndi kundiuza mabodza; undiuze tsopano,
ndikupempha, cimene angakumange naco. 11Nanena naye,
Akandimangitsa nazo zingwe zatsopano, zosagwira nazo nchito
pamenepo ndidzakhala: wofoka wakunga munthu wina. 12Ndipo
Delila anatenga nsinga zatsopano, nammanga nazo, nanena naye,
Atilisti akugwera, Samsoni. Ndi omlalira analikulinda m'cipinda ca
m'kati. Koma anazidula pa manja ace ngati thonje. 13Pamenepo
Delila anati kwa Samsoni, Mpaka tsopano wandipusitsa, ndi
kundiuza mabodza; undiuze cimene angakumange naco. Nanena
naye, Ukaomba njombi zisanu ndi ziwiri za pamutu panga mwa
thonje loyala ndiko. 14Ndipo anacimanga ndi phanga, nati kwa iye,
Akugwera Afilisti, Samsoni; nagalamuka iye patulo tace, nazula
phanga la pamtanda, ndi thonje loyala lomwe. 15Pamenepo
ananena naye, Ukati bwanji, Ndikukonda, osamvana nane mtima
wako? wandipusitsa katatu tsopano, osandiuza umo mucokera
mphamvu yako yaikuru, 16Ndipo kunali, popeza anamuumiriza
masiku onse ndi mau ace, oamkakamiza, moyo wace unabvutika

nkufuna kufa. 17Pomwepo anamfotokozera mtima wace wonse,
nanena naye, Pamutu panga sipanapite lumo, pakuti ndine Mnaziri
wa Mulungu ciyambire mimba ya mai wanga; akandimeta,
mphamvu yanga idzandicokera, ndidzakhala wofoka wakunga
munthu wina ali yense. 18Ndipo pamene Delila anaona kuti
adamfotokozera mtima wace wonse, anatuma naitana akalonga a
Afilisti, ndi kuti, Kwerani nthawi yino, pakuti wandifotokozera za
mtima wace wonse. Nakwera akalonga a Afilisti nadza kwa iye
nabwera nazo ndalamazo m'dzanja lao. 19Pamenepo anamgonetsa
pa mabondo ace, naitana munthu, nameta njombi zace zisanu ndi
ziwiri; nayamba kumzunza, nimcokera mphamvu yaceo 20Ndipo
anati, Afilisti akugwera, Samsoni. Nagalamuka iye m'tulo tace,
nati, Ndizituruka ngati nthawi zina, ndi kudzitakasika. Koma
sanadziwa kuti Yehova adamcokera. 21Pamenepo Afilisti
anamgwira, namkolowola maso, natsika naye ku Gaza, nammanga
ndi maunyolo amkuwa; namperetsa m'kaidi. 22Koma atammeta
tsitsi la pamutu pace linayamba kumeranso.

Samsoni agwetsa nyumba ya Dagoni

23Ndipo anasonkhana akalonga a Afilisti kuperekera Dagoni
mulungu wao nsembe yaikuru, ndi kusekerera; pakuti anati,
Mulungu wathu wapereka Samsoni mdani wathu m'dzanja
lathu. 24Ndipo pakumuona anthu analemekeza mulungu wao,
pakuti anati, Mulungu wathu wapereka m'dzanja lathu mdani
wathu, ndiye wakupasula dziko lathu, amene anatiphera
ambiri. 25Ndipo kunali, pakukondwera mitima yao, anati, Kaitaneni
Samsoni, atisewerere. Naitana Samsoni m'kaidi; nasewera iye
pamaso pao; ndipo anamuika iye pakati pa mizati. 26Ndipo
Samsoni anati kwa mnyamata womgwira dzanja, Ndileke,
ndikhudze mizati imene nyumba ikhazikikapo, kuti
nditsamirepo. 27Koma nyumbayi inadzala ndi amuna ndi akazi; ndi
akalonga onse a Afilisti anali momwemo ndi patsindwi panali
amuna ndi akazi ngati zikwi zitatu akuyang'ana pakusewera
Samsoni. 28Pamenepo Samsoni anaitana kwa Yehova, nati, Yehova,
Mulungu, dikupempha mundikumbukile, ndikupemphani, ndi
kundilimbitsa, ndikupemphani, nthawi yino yokha, Mulungu, kuti
ndidzilipsiriretu tsopano apa Afilisti, cifukwa ca maso anga
awiri. 29Ndipo Samsoni anagwira mizati iwiri ya pakati imene
nyumba inakhazikikapo, natsamirapo wina ndi dzanja lamanja, ndi
unzace ndi dzanja lamanzere. 30Nati Samsoni, Ndife nao Afilisti;
nadziweramira mwamphamvu; ndipo nyumba idagwa pa akalonga,
ndi pa anthu onse anali m'mwemo. Motero akufa amene anawapha
pa kufa kwace anaposa amene anawapha akali moyo. 31Pamenepo
anatsika abale ace ndi banja lonse la atate wace, namnyamula,

Dakwera naye, namuika pakati pa Zora ndi Esitaoli, m'manda a Manowa atate wace. Ndipo adaweruza Israyeli zaka makumi awiri.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Mika ndi fano lace

1Ndipo ku mapiri a Efraimu kunali munthu dzina lace ndiye
Mika. 2Ndipo iye anati kwa amai wace, Ndarama zija mazana
khumi ndi limodzi anakuberani zimene munatembererapo, ndi
kunenanso m'makutu mwanga, taonani ndaramazo ndiri nazo,
ndinazitenga ndine. Pamenepo amai wace anati, Yehova adalitse
mwana wanga. 3Nabwezera amace ndarama zija mazana khumi
ndi limodzi; nati amai wace, Kupatula ndapatulira Yehova
ndaramazo zicoke ku dzanja langa, zimuke kwa mwana wanga,
kupanga nazo dikupempha fano losema ndi fane loyenga;
m'mwemo ndikubwezera izi. 4Ndipo pamene anambwezera mai
wace ndaramazo, mai wace anatapako ndarama mazana awiri,
nazipereka kwa woyenga, ndiye anazipanga fane losema ndi fano
loyenga; ndipo linakhala m'nyumba ya Mika. 5Koma munthuyu
Mika anali nayo nyumba ya milungu, napanga cobvala ca
wansembe, ndi timafano, namninkha zansembe mwana wace wina
wamwamuna, amene anakhala wansembe wace. 6Masikuwa
panalibe mfumu m'Israyeli, yense anacita comuyenera m'maso
mwace.
7Ndipo panali mnyamata wa ku Betelehemu-Yuda wa banja la Yuda,
ndiye Mlevi, nagonera iye komweko. 8Adacokera munthuyo
m'mudzi m'Betelehemu-Yuda, kugonera pali ponse akapeza
pokhala; ndi pa ulendo wace anafika ku mapiri a Efraimu, ku
nyumba ya Mika. 9Ndipo Mika ananena naye, Ufumira kuti? Nati
kwa iye, Ndine Mlevi wa ku Betelehemu-Yuda, ndirikumuka
kugonera kumene ndikapeza pokhala. 10Nanena naye Mika,
Khalitsa nane, nukhale atate wanga, ndi wansembe wanga, ndipo
ndidzakupatsa ndarama khumi pacaka, ndi cobvala cofikira, ndi
zakudya zako. Nalowa Mleviyo. 11Ndi Mleviyo anabvomera
kukhalitsa ndi munthuyo; ndi mnyamatayo anamkhalira ngati
mmodzi wa ana ace. 12Ndipo Mika anamninkha zansembe Mleviyo,
ndi mnyamatayo anakhala wansembe wace, nakhala m'nyumba ya
Mika. 13Nati Mika, Tsopano ndidziwa kuti Yehova adzandicitira
cokoma, popeza ndiri naye Mlevi akhale wansembe wanga.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Ana a Dani alanda mafano a Mika

1Masiku ajawo panalibe mfumu m'Israyeli; masiku ajanso pfuko la
Adani anadzifunira colowa cakukhalako; pakuti kufikira tsiku lija
sicinawagwera colowa cao pakati pa mapfuko a Israyeli. 2Ndipo
ana a Dani anatuma a banja lao amuna asanu a mwa iwo onse,
anthu olimba mtima, a ku Zora, ndi a ku Esitaoli, a kuzonda dziko
ndi kufunafunamo; nanena nao, Mukani, mufunefune m'dziko.
Nafika iwo ku mapiri a Efraimu ku nyumba ya Mika, nagona
komweko, 3Pokhala iwo m'nyumba ya Mika, anazindikira mau a
mnyamata Mleviyo, napambukirako, nanena naye, Anadza nawe
kuno ndani? ucitanji muno? ukhala naco ciani kuno? 4Ndipo
ananena nao, Mika anandicitira cakuti cakuti, napangana nane za
nchito, ndipo ndikhala wansembe wace. 5Pamenepo ananena
naye, Utifunsire kwa Mulungu, kuti tidziwe ngati ulendo wathu
timukawo udzakoma. 6Nanena nao wansembeyo, Mukani
mumtendere, ulendo wanu muyendawo uli pamaso pa Yehova.
7Pamenepo amuna asanuwa anacoka, nafika ku Laisi; naona anthu
anali m'mwemo, kuti anakhalaokhazikika mtima, monga anakhala
Asidoni, odekha ndi osatekeseka; popeza m'dzikomo munalibe
mwini bwalo wakudtitsa manyazi m'cinthu ciri conse; nasiyana
kutali ndi Asidoni, ndipo analibe kanthu ndi munthu ali
yense. 8Ndipo asanuwo anafikanso kwa abale ao ku Zora ndi
Esitaoli; ndi abale ao ananena nao, Mutani inu? 9Nati iwo, Taukani,
tiwakwerere; pakuti tapenya dziko, ndipo taonani, ndilo lokoma
ndithu; ndi inu muli cete kodi? musamacita ulesi kumuka ndi
kulowa kulandira dzikolo, 10Pomuka inu mudzafikira anthu
okhazikika mtima ndi dziko ladtando; pakuti Mulungu walipereka
m'dzanja lanu; pamenepo mposasowa kanthu kali konse kali pa
dziko lapansi.
11Pamenepo amuna mazana asanu ndi limodzi, omangira zida za
nkhondo m'cuuno, anaphumulako a banja la a Dani, anacokera ku
Zora, ndi ku Esitaoli. 12Nakwera namanga misasa m'Kiriyati-
yearimu, m'Yuda; cifukwa cace anacha dzina lace la malowo
cigono ca Dani, mpaka lero; taona, ali m'tseri mwa
Kiriyatiyearimu. 13Ndipo anapiririra komweko kumka ku mapiri a
Efraimu, nadza ku nyumba ya Mika. 14Pamenepo anayankha
amuna asanu anamukawo kukazonda dziko la Laisi, nanena ndi
abale ao, Kodi mudziwa kuti m'nyumba izi muli cobvala ca
wansembe, ndi timafano ndi fano losema, ndi fano loyenga? Ndipo
tsopano dziwani coyenera inu kucita. 15Napambuka iwo kumkako,
nafika ku nyumba ya mnyamata Mleviyo, ndiyo nyumba ya Mika,
namfunsa ngati ali bwanji. 16Ndipo amuna mazana asanu ndi
limodzi omangira zida zao za nkhondo m'cuuno, ndiwo a ana a-

Dani, analikuima polowera pa cipata; 17koma amuna asanu
omukawo kukazonda dziko anakwera nalowako, natenga fano
losema, ndi cobvala ca wansembe ndi timafano, ndi fano loyenga;
ndi wansembe anaima polowera pa cipata pamodzi ndi amuna
mazana asanu ndi limodzi omangira zida za nkhondo
m'cuuno. 18Atalowa iwo m'nyumba ya Mika, natengako fane
losema, cobvala ca wansembe, ndi timafano, ndi fano loyenga,
wansembeyo ananena nao, Mucitanji? 19Ndipo ananena naye,
Khala cete, tseka pakamwa pako, numuke nafe, nutikhalire atate
ndi wansembe wathu; cikukomera nciti, kukhala wansembe wa
nyumba ya munthu mmodzi, kapena kukhala wansembe wa pfuko
ndi banja m'Israyeli? 20Nukondwera mtima wa wansembeyo,
natenga iye cobvala ca wansembe, ndi timafano ndi fano losema,
nalowa pakati pa anthu. 21Atatero anabwerera, nacoka, natsogoza
ana ang'ono ndi zoweta ndi akatundu. 22Atafika kutari ndi nyumba
ya Mika, Mikayo anawamemeza amuna a m'nyumba zoyandikizana
ndi yace, natsata ndi kuwapeza ana a Dani. 23Ndipo anapfuula kwa
ana a Dani. Naceuka iwo nati kwa Mika, Cakusowa ciani, kuti
wamemeza anthu ako? 24Nati iye, Mwanditengera milungu yanga
ndinaipanga, ndi wansembe, ndi kucoka; cinditsaliranso ciani?
ndipo muneneranji kwa ine, Cakusowa nciani? 25Koma ana a Dani
anati kwa iye, Mau ako asamveke ndi ife, angakugwere anthu
owawa mtima, nukataya moyo wako ndi wa iwo a m'nyumba
mwako. 26Nayenda ulendo wao ana a Dani; ndipo Mika pakuona
kuti anamposa mphamvu, anatembenuka nabwerera kunyumba
kwace. 27M'mwemo anatenga zimene Mika adacipanga, ndi
wansembe anali naye, nafika ku Laisi, kwa anthu odekha ndi
okhazikika mtima, nawakantha ndi lupanga lakuthwa, natentha
mudzi wao ndi moto. 28Ndipo panalibe wolanditsa, popeza ku
Sidoni nkutali, ndipo analibe kuyenderana ndi anthu ena; ndiko ku
cigwa cokhala ku Betirehobo. Pamenepo anamanganso mudziwo,
nakhala m'mwemo. 29Ndipo analicha dzina la mudziwo Dani,
kutsata dzina la atate wao Dani wombala Israyeli; koma
poyambapo dzina la mudzi linali Laisi. 30Ndipo ana a Dani
anadziimitsira fane losemalo; ndi Yonatani mwana wa Gerisomu
mwana wa Manase, iye ndi ana ace amuna anali ansembe a pfuko
la Adani mpaka tsiku lija anatenga ndende anthu a
m'dziko. 31Motero anadziikira fane losema la Mika, limene
adalipanga, masiku onse okhala nyumba ya Mulungu ku Silo.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Coopsa adacicita a ku Gibeya

1Ndipo kunali, masiku aja, pamene panalibe mfumu m'Israyeli,
panali munthu Mlevi wogonera kutseri kwa mapiri a Efraimu
amene anadzitengera mkazi wamng'ono wa ku Betelehemu-
Yuda. 2Koma mkazi wace wamng'ono anacita cigololo akali naye,
namcokera kumka ku nyumba ya atate wace ku Betelehemu-Yuda,
nakhalako nthawi ya miyezi inai. 3Koma anauka mwamuna wace
namtsata kukamba naye zamtima, kumbwezanso; napita ndi
mnyamata wace, ndi aburu awiri. Ndipo mkaziyo anadza naye ku
nyumba ya atate wace. Ndipo pakumuona atate wa mkaziyo,
anakondwera kukomana naye. 4Ndipo mpongozi wace, ndiye atate
wa mkaziyo, anamuimika kuti akhale naye masiku atatu; nadya
namwa nagona komweko. 5Ndipo kunali, tsiku lacinai, analawirira
mamawa, nanyamuka iye kucoka; koma atate wa mkaziyo anati
kwa mkamwini wace, Limbitsa mtima wako ndi mkate pang'ono,
ndipo utatero upite. 6Nakhala pansi nadya namwa onse awiri
pamodzi; nati kwa munthuyo atate wa mkaziyo, Ubvomere, ugone
kuno usiku, nusekerere mtima wako. 7Ndipo munthuyo
ananyamuka kuti amuke; koma mpongozi waceyo anamkakamiza,
nagonanso komweko. 8Nalawirira mamawa tsiku lacisanu kuti
amuke, koma atate wa mkaziyo anati, Ulimbitse mtima wako,
nulindire lipendeke dzuwa; nadya iwo onse awiri. 9Pamenepo
munthuyo ananyamuka kucoka, iye ndi mkazi wace wamng'ono
ndi mnyamata wace; koma mpongozi wace, atate wa mkaziyo,
ananena naye, Tapenya, lapendeka dzuwa, ugone kuno usiku;
tapenya lapendekatu dzuwa, ugone kuno, nusekerere mtima wako;
nimulawire mamawa kumka ulendo wanu kwanu. 10Koma
munthuyo anakana kugonako usiku, nanyamuka, nacoka, nadza
pandunji pa Yebusi (ndiwo Yerusalemu); ndi pamodzi naye panali
aburu awiri omangirira mbereko; anali nayenso mkazi wace
wamng'ono. 11Pofika iwo pa Yebusi linalimkulowa dzuwa, ndi
mnyamata anati kwa mbuye wace, Tiyeni, tipambukire mudzi uwu
wa Ayebusi ndi kugona pomwepa. 12Koma mbuye wace ananena
naye, Tisapambukire mudzi wacilendo, wosati wa ana a Israyeli,
koma tipitirire kumka ku Gibeya, 13Nati kwa mnyamata wace,
Tiyeni, tiyandikire kwinako: tigone m'Gibeya, kapena
m'Rama. 14Napitiriraiwo, nayenda, ndi dzuwa linawalowera pafupi
pa Gibeya, ndiwo wa Benjamini. 15Napambukirako, kuti alowe
nagone ku Gibeya; nalowa iye, nakhala pansi m'khwalala la
mudziwo, pakuti panalibe wina wowalandira m'nyumba agonemo,
wakuwapatsa pogona. 16Ndipo taonani, munthu nkhalamba
anacokera ku nchito yace kumunda madzulo; munthuyu ndiye wa
ku mapiri a Efraimu, nagonera ku Gibeya; kuma anthu pamenepo

ndiwo Abenjamini. 17Pamene anakweza maso ace anaona munthu wa pa ulendoyo m'khwalala la mudzi; ndi nkhalambayo inati, Umuka kuti? ufumira kuti? 18Ndipo ananena nayo, Tirikucokera ku BetelehemuYuda, kumka ku mbali za mapiri a Efraimu, ndiko ndifumira ine; koma ndidamuka ku Betelehemu-Yuda; ndipo tsopano ndiri kumuka ku nyumba ya Yehova; koma palibe munthu wondipatsa nyumba. 19Ngakhale maudzu ndi cakudya ca aburu athu ziriko; ndi mkate ndi vinyo zirikonso kwa ine ndi kwa mdzakazi wako ndi kwa mnyamata wokhala ndi aka polo ako; kosasowa kanthu. 20Ndipo nkhalambayo inati, Mtendere ukhale ndi iwe, komatu, zosowa zako zonse ndidzakuparsa ndi ine; pokhapo usa gone m'khwalala. 21Pamenepo anamlonga m'nyumba yace, napatsa aburu cakudya; ndipo iwo anasamba mapazi ao, nadya, namwa. 22Pokondweretsa iwo mitima yao, taonani amuna a m'mudziwo, ndiwo anthu otama zopanda pace, anazinga nyumba, nagogodagogoda pacitseko; nati kwa mwini nyumba nkhalambayo ndi kuti, Turutsa mwamunayo adalowa m'nyumba mwako kuti timdziwe. 23Ndipo munthu mwini nyumba anawaturukira nanena nao, lai, abale anga, musacite coipa cotere; popeza mwamuna uyu walowa m'nyumba mwanga, musacite copusa ici. 24Taonani, mwana wanga wamkazi ndiye namwali, ndi mkazi wace wamng'onoyo siwa; ndiwaturutse iwo, muwacepetse iwo, ndi kuwacitira monga muyesa cokoma; koma mwamuna uyu musamcitire copusa ici. 25Koma amunawo sanafuna kumvera; motero munthuyu anagwira mkazi wace wamng'ono, naturuka naye kwa iwo kunja; namdziwa iwo, nacita naye zoipa usiku wonse mpaka m'mawa; namlola acoke mbandakuca. 26Nadza mkaziyo kutaca, nagwa pakhomo pa nyumba ya munthu padali mbuye wace, kufikira kutayera. 27Pamene mbuye wace anauka mamawa, natsegula pakhomo pa nyumba, naturuka kumka ulendo wace, taona, mkazi wace wamng'onoyo, atagwa pakhomo pa nyumba ndi manja ace paciundo. 28Ndipo ananena naye, Tauka, timuke; koma panalibe womyankha. Pamenepo anamuika pa buru; nanyamuka mwamunayo, namka kwao. 29Ndipo pofika iye kunyumba kwace, anatenga mpeni, nagwira mkazi wace wamng'onoyo namgawa ciwalo ciwalo magawo khumi ndi awiri, namtumiza ku mame onse a Israyeli. 30Ndipo kunali kuti onse amene anaciona anati, Sicinacitika, inde sicinaoneka cotere ciyambire tsiku lokwera ana a Israyeli kuturuka m'dziko la Aigupto mpaka lero lino; lingiriranipo, mupangane nzeru, nimunene.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Aisrayeli abwezera cilango pfuko la Benjamini

1Pamenepo anaturuka ana onse a Israyeli, nuunjikana msonkhano
kwa Yehova ku Mizipa ngati munthu mmodzi, kuyambira ku Dani
mpaka Beereseba ndi dziko la Gileadi lomwe. 2Ndipo akuru a anthu
onse a mapfuko onse a Israyeli anadziimika mu msonkhano wa
anthu a Mulungu, anthu oyenda pansi zikwi mazana anai akusolola
lupanga, 3Ndipo ana a Benjamini anamva kuti ana a Israyeli
adakwera kumka ku Mizipa, Nati ana a Israyeli, Nenani, coipa ici
cinacitika bwanji? 4Ndipo Mlevi, mwamuna wa mkazi
anaphedwayo, anayankha nati, Ndinadza ine ku Gibeya wa
Benjamini, ine ndi mkazi wanga wamng'ono,
kugonako. 5Nandiukira eni ace a Gibeya, nandizingira nyumba
usiku; nafuna kundipha ine, namcitira coipa mkazi wanga
wamng'ono, nafa iye, 6Pamenepo ndinagwira mkazi wanga
wamng'ono ndi kumgawa ndi kumtumiza m'dziko lonse la colowa
ca Israyeli, pakuti anacita cocititsa manyazi ndi copusa
m'Israyeli. 7Taonani, inu nonse, ndinu ana a Israyeli, mudzinenere
mau ndi kudzipangira nokha kuno. 8Ndipo anthu onse anauka ngati
munthu mmodzi, ndi kuti, Palibe mmodzi wa ife adzamuka kuhema
kwace, kapena kupambukira nyumba yace, 9koma tsopano ici
ndico tidzacitira Gibeya: tidzaukwerera ndi kulota maere. 10Ndipo
tidzatapa amuna khumi limodzi pa zana limodzi, mwa mapfuko
onse a Israyeli; ndi zana limodzi pa zikwi cimodzi, ndi cikwi cimodzi
pa zikwi khumi kutengera anthu kamba; kuti pakufika ku Gibeya
wa Benjamini, aucitire monga mwa copusa conse unacita
m'Israyeli. 11Potero amuna onse a Israyeli anasonkhanira mudziwo,
olunzika ngati munthu mmodzi.
12Ndipo mapfuko a Israyeli anatuma anthu mwa pfuko lonse la
Benjamini, ndi kuti, Coipa canji ici cinacitika mwa inu? 13Ndipo
tsopano perekani amunawo otama zopanda pace, okhala
m'Gibeya, kuti tiwaphe, ndi kucotsera Israyeli coipaci. Koma
Benjamini sanafuna kumvera mau a abale ao, ana a
Israyeli. 14Ndipo ana a Benjamini anasonkhana kucokera ku midzi
kumka ku Gibeya, kuti aturuke kulimbana ndi ana a
Israyeli. 15Ndipo anawerenga ana a Benjamini a m'midzi tsiku lija
amuna zikwi makumi awiri mphambu zisanu ndi cimodzi akusolola
lupanga; osawerenga okhala m'Gibeya, ndiwo amuna osankhika
mazana asanu ndi awiri. 16Mwa anthu awa onse munali amuna
osankhika mazana asanu ndi awiri amanzere, yense wa iwo
amaponya mwala mwa maluli osaphonya. 17Ndipo anawerenga
amuna a Israyeli, osati Benjamini, amuna zikwi mazana anai
osolola lupanga, anthu a nkhondo okha okha. 18Nauka ana a
Israyeli, nakwera kumka ku Beteli, nafunsira kwa Mulungu, nati,

Ayambe ndani kutikwerera pa ana a Benjamini? Ndipo Yehova anati, Ayambe ndi Yuda. 19Nauka ana a Israyeli m'mawa, naumangira Gibeya misasa. 20Ndipo amuna a Israyeli anaturuka kulimbana ndi Benjamini; ndi amuna a Israyeli anawandandalikira nkhondo ku Gibeya. 21Pamenepo ana a Benjamini anaturuka m'Gibeya, naononga a Israyeli tsiku lija zikwi makumi awiri mphambu ziwiri, kuwagoneka pansi, 22Koma anthu, ndiwo amuna a Israyeli, anadzilimbitsa nanikanso nkhondo kumene anandandalika tsiku loyambalo. 23Ndipo ana a Israyeli anakwera nalira misozi pamaso pa Yehova mpaka madzulo; nafunsira kwa Yehova ndi kuti, Ndiyandikizenso kodi kulimbana nkhondo ndi ana a Benjamini mbale wanga? Ndipo Yehova anati, Mumkwerere.
24Potero ana a Israyeli anayandikira ana a Benjamini m'mawa mwace. 25Ndipo Benjamini anawaturukira ku Gibeya m'mawa mwace, naononganso a ana a Israyeli amuna zikwi khumi ndi zisanu ndi zitatu kuwagoneka pansi; ndiwo onse osolola lupanga. 26Pamenepo ana onse a Israyeli ndi anthu onse anakwera nafika ku Beteli, nalira misozi, nakhala pansi pomwepo pamaso pa Yehova, nasala cakudya tsiku lomwelo mpaka madzulo; napereka nsembe zopsereza ndi nsembe zoyamika pamaso pa Yehova. 27Ndipo ana a Israyeli anafunsira kwa Yehova; pakuti likasa la cipangano la Mulungu linakhala komweko masiku aja, 28namaima ku likasalo Pinehasi mwana wa Eleazare mwana wa Aroni, masiku aja; nati, Kodi nditurukenso kulimbana nkhondo ndi ana a Benjamini mbale wanga, kapena ndileke Ndipo Yehova anati, Kwerani, pakuti mawa ndidzampereka m'dzanja lako. 29Ndipo Israyeli anaika olalira Gibeya pozungulira pace.
30Ndipo ana a Israyeli anakwerera ana a Benjamini tsiku lacitatu, na nika pa Gibeya monga nthawi zina. 31Naturuka ana a Benjamini kukomana ndi anthuwo, nakokedwa kutali ndi mudzi, nayamba kuwakantha ndi kuwapha anthu amuna a Israyeli, ngati makumi atatu monga nthawi zina, m'makwalala, limodzi la awo lokwera kumka ku Beteli, ndi lina ku Gibeya kuthengo. 32Ndipo ana a Benjamini anati, Tawakantha pamaso pathu monga poyamba paja. Koma ana a Israyeli anati, Tithawe, tiwakokere kutari ndi mudzi kumakwalala. 33Nauka amuna onse a Israyeli m'malo ao nanika ku Baalatamari; naturuka Aisrayeli olalira aja m'malo mwao, m'Maare-geba. 34Ndipo anadza pandunji pa Gibeya amuna osankhika m'Israyeli monse zikwi khumi, nikula nkhondo; koma sanadziwa kuti coipa ciri pafupi kuwakhudza. 35Ndipo Yehova anakantha Benjamini pamaso pa Israyeli; ndi ana a Israyeli anawaononga a Benjamini tsiku lija amuna zikwi makumi awiri ndi zisanu, kudza zana limodzi; awa onse ndiwo akusolola lupanga.

36Ndipo ana a Benjamini anaona kuti takanthidwa; popeza amuna
a Israyeli anawapatsa Abenjamini malo, pakuti anatama olalira
amene anawaikiratu pa Gibeya. 37Nafulumira olalirawo
nathamangira Gibeya, nabalalika olalirawo, nakantha mudzi wonse
ndi lupanga lakuthwa. 38Koma kunali cizindikilo coikika pakati pa
amuna a Israyeli ndi olalirawo, ndico cakuti afukitse mtambo wa
utsi kumudzi. 39Ndi nkhondo ya Israyeli inathawa, ndipo Benjamini
anayamba kuwakantha ndi kuwagwaza amuna a Israyeli, ngati
amuna makumi atatu, pakuti anati, Ndithu Tawakantha konse
pamaso pathu, monga ku nkhondo yoyambayo. 40Koma pamene
mtambo unayamba kukwera m'mudzi ngati utsi uti tolo,
Abenjamini anaceuka, ndipo taonani, pamodzi ponse panafuka utsi
kumwamba. 41Natembenuka amuna a Israyeli; nadabwa amuna a
Benjamini; popeza anaona kuti cidawagwera coipa. 42Nabwerera
iwo pamaso pa amuna a Israyeli kumka njira ya cipululu; koma
nkhondo inawaloodetsa; ndi aja oturuka m'mudzi anawaononga
pakati pao. 43Anawazinga Abenjamini, anawapitikitsa,
nawapondereza pampumulo mpaka pandunji pa Gibeya, koturukira
dzuwa. 44Ndipo adagwa a Benjamini amuna zikwi khumi ndi zisanu
ndi zitatu; iwo onse ndiwo ngwazi. 45Natembenuka iwo, nathawira
kucipululu ku thanthwe la Rimoni; koma anawakunkha
m'makwalala amuna zikwi zisanu; nawalondetsa ku Gidomu,
nakantha a iwowa amuna zikwi ziwiri. 46Potero onse amene
adagwa a Benjamini tsiku lija, ndiwo amuna zikwi makumi awiri
mphambu zisanu, akusolola lupanga; iwo onse ndiwo
ngwazi. 47Koma amuna mazana asanu ndi limodzi anabwerera
nathawira kucipululu, ku thanthwe la Rimoni, nakhala m'thanthwe
la Rimoni miyezi inai. 48Ndipo amuna a Israyeli anabwereranso
kwa ana a Benjamini, nawakantha ndi lupanga lakuthwa a m'mudzi
wonse, ndi zoweta, ndi zonse adazipeza; anatenthanso midzi
yonse anaipeza.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Pfuko la Benjamini limangidwanso

1Koma amuna a Israyeli adalumbira ku Mizipa, ndi kuti, Palibe
mmodzi wa ife adzapereka mwana wace wamkazi kwa Mbenjamini
akhale mkazi wace. 2Ndipo anthu anadza ku Beteli, nakhala pansi
pomwepo pamaso pa Mulungu mpaka madzulo; nakweza mau ao
ndi kulira misozi yambiri. 3Nati iwo, Yehova Mulungu wa Israyeli,
cacitika ici cifukwa ninji m'Israyeli kuti lasowa lero pfuko limodzi
m'Israyeli? 4Ndipo kunali m'mawa mwace, anthu analawirira
mamawa namangako guwa la nsembe, napereka nsembe
zopsereza ndi nsembe zoyamika. 5Nati ana a Israyeli, Ndani iye
mwa mapfuko onse a Israyeli amene sanakwera kudza
kumsonkhano kwa Yehova? pakuti panali lumbiro lalikuru pa iye
wosakwera kudza kwa Yehova ku Mizipa, ndi kuti, Aphedwe
ndithu. 6Ndipo ana a Israyeli anamva cifundo cifukwa ca Benjamini
mbale wao, nati, Pfuko limodzi lalikhidwa pa Israyeli
leroli. 7Tidzatani kuwafunira otsalawo akazi, popeza tinalumbira ife
pa Yehova kuti sitidzawapatsa ana athu akazi akhale akazi
ao? 8Nati iwo, Kodi pali lina la mapfuko a Israyeli losakwera kudza
kwa Yehova ku Mizipa? Ndipo taonani, kucokera ku Yabesi-gileadi
sanadza mmodzi kumisasa, kumsonkhano. 9Pakuti pamene
anawerenga anthu, taonani, panalibe mmodzi komweko wa okhala
m'Yabesi-gileadi, 10Ndipo msonkhano unatumizako amuna zikwi
khumi ndi ziwiri, ndiwo ngwazi, nawalamulira ndi kuti, Mukani,
nimuwakanthe okhala m'Yabesi-gileadi ndi lupanga lakuthwa, ndi
akazi ndi ana ang'ono. 11Ndipo cimene mukacite ndi ici:
mukaononge konse mwamuna ali yense, ndi mkazi ali yense
wodziwa mwamuna mogona naye. 12Ndipo anapeza mwa anthu a
Yabesi-gileadi anamwali mazana anai osadziwa mwamuna mogona
naye; nabwera nao kumisasa ku Silo, ndiwo a m'dziko la Kanani.
13Ndipo msonkhano wonse unatumiza mau kwa ana a Benjamini
okhala m'thanthwe la Rimoni, nawalalikira mtendere. 14Nakwera
Abenjamini nthawi ija, ndipo anawapatsa akazi amene
anawasunga amoyo mwa akazi a Yabesi-gileadi; koma
sanawafikira. 15Ndipo anthu anamva cifundo pa Benjamini, pakuti
Yehova adang'amba mapfuko a Israyeli.
16Pamenepo akuru a msonkhano anati, Tidzatani, kuwafunira akazi
otsalawo, popeza akazi anatha psiti m'Benjamini? 17Nati iwo,
Pakhale colowa ca iwo opulumuka a Benjamini, lingafafanizidwe
pfuko m'Israyeli. 18Koma sitikhoza ife kuwapatsa ana athu akazi
akhale akazi ao; pakuti ana a Israyeli adalumbira ndi kuti,
Atembereredwe wakupatsa Abenjamini mkazi. 19Natiiwo, Taonani,
pali madyerero a Yehova caka ndi caka ku Silo, ndiko kumpoto kwa
Beteli, kum'mawa kwa mseu wokwera kucokera ku Beteli kumka ku

Sekemu, ndi kumwela kwa Lebona. 20Ndipo analamulira ana a
Benjamini ndi kuti, Mukani, mulalire m'minda
yamphesa; 21nimuyang'ane, ndipo taonani, ataturuka ana akazi a
Silo kubvinabvina, pamenepo muturuke m'minda yamphesa ndi
kudzigwirira yense mkazi wace mwa ana akazi a Silo, ndi kumuka
naye ku dziko la Benjamini. 22Ndipo kudzali, akatifikira atate ao
kapena alongo ao kunena nafe mlandu, tidzanena nao, Mutipatse
awa, pakuti sitinawatengera yense mkazi wace kunkhondo; pakuti
inunso simunawaninkha awa; mukadatero mukadaparamula
tsopano. 23Nacita cotere ana a Benjamini, nadzitengera akazi
monga mwa kuwerenga kwao, a obvina aja, amene anawatenga
mwacifwamba; namuka iwo nabwerera ku colowa cao, namanga
midzi, nakhalamo. 24Ndipo ana a Israyeli anacokako nthawi ija
yense kumka ku pfuko lace, ndi banja lace, naturukako yense
kumka ku colowa cace. 25Panalibe mfumu m'Israyeli masiku aja; a
yense anacita comkomera pamaso pace.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Ruth

Rute 1

Naomi ndi apongozi ace awiri

1NDIPO masiku akuweruza oweruzawo munali njala m'dziko. Ndipo munthu wa ku Betelehemu-Yuda anamuka nakagonera m'dziko la Moabu, iyeyu, ndi mkazi wace, ndi ana ace amuna awiri. 2Dzina la munthuyo ndiye Elimeleki, ndi dzina la mkazi wace ndiye Naomi, ndi maina a ana ace awiri ndiwo Maloni, ndi Kilioni; ndiwo a ku Efrata ku Betelelehemu-Yuda. Iwowa ndipo analowa m'dziko la Moabu, nakhala komweko. 3Ndipo Elimeleki mwamuna wace wa Naomi anamwalira; natsala iye ndi ana ace awiri. 4Nadzitengera iwo akazi a ku Moabu; wina dzina lace ndiye Olipa, mnzace dzina lace ndiye Rute; ndipo anagonera komweko ngati zaka khumi. 5Koma Maloni ndi Kilioni anamwalira onse awiri; motero ana ace amuna awiri ndi mwamuna wace anamsiya mkaziyo. 6Pamenepo ananyamuka iyeyu ndi apongozi ace kuti abwerere kucoka m'dziko la Moabu; pakuti adamva m'dziko la Moabu kuti Yehova adasamalira anthu ace ndi kuwapatsa cakudya. 7Naturuka iye kumene anakhalako ndi apongozi ace awiri pamodzi naye; namka ulendo wao kubwererakudzikola Yuda. 8Ndipo Naomi anati kwa apongozi ace awiri, Mukani, bwererani yense wa inu ku nyumba ya amai wace; Yehova akucitireni zokoma, monga umo munacitira akufa aja ndi ine. 9Yehova akuloleni mupeze mpumulo yense m'nyumba ya mwamuna wace. Nawapsompsona, nakweza iwo mau ao nalira misozi. 10Ndipo ananena naye, Iai, koma tidzapita nanu kwa anthu a kwanu. 11Nati Naomi, Bwererani, ana anga, mudzatsagana nane bwanji? ngati ndiri nao m'mimba mwanga ana amuna ena kuti akhale amuna anu? 12Bwererani, ana anga, mukani, pakuti ndakalambitsa ine, sindikhoza kukhala naye mwamuna. Ngakhale ndikati, Ndiri naco ciyembekezo, ndikakhala naye mwamuna usiku uno, ndi kubalanso ana amuna; 13kodi mudzawalindirira akakula? mudzadziletsa osakwatibwa? Iai, ana anga, pakuti candiwawa koposa cifukwa ca inu popeza dzanja la Yehova landiturukira. 14Nakweza iwo mau ao, naliranso misozi; ndi Olipa anampsompsona mpongozi wace, koma Rute anamkangamira. 15Pamenepo anati, Taona mbale wako wabwerera kwa anthu a kwao, ndi kwa mulungu wace, bwerera umtsate mbale wako. 16Nati Rute, Musandiumirize kuti ndikusiyeni, ndi kubwerera osakutsatani; pakuti kumene mumukako ndimuka inenso, ndi kumene mugonako ndigona inenso; anthu a kwanu ndiwo anthu a kwa inenso, ndi Mulungu wanu ndiye Mulungu wanga; 17kumene mudzafera inu ine ndidzafera komweko, ndi

kuikidwa komweko; andilange Yehova naonjezeko, ciri conse cikasiyanitsa inu ndi ine, koma imfa ndiyo. 18Ndipo pakuona kuti analimbika kumuka naye, analeka kulankhula naye. 19Namuka iwo awiriwo mpaka anafika ku Betelehemu. Ndipo kunali pakufika iwo ku Betelehemu, mudzi wonse unapokosera za iwo; nati, Kodi uyu ndi Naomi? 20Koma ananena nao, Musandicha Naomi, mundiehe Mara; pakuti Wamphamvuyonse anandicitira zowawa ndithu. 21Ndinacoka pane wolemera, nandibwezanso kwathu Yehova wopanda kanthu; mundicheranji Naomi, popeza Yehova wandicitira umboni wakunditsutsa, ndi Wamphamvuyonse wandicitira cowawa? 22Momwemo anabwera Naomi ndi Rute Mmoabu mpongozi wace pamodzi naye, amene anabwera kucokera ku dziko la Moabu; ndipo anafika ku Betelehemu, pakuyamba anthu kuceka barele.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Rute akunkha m'munda wa Boazi

1Ndipo Naomi anali nave mbale wa mwamuna wace, ndiye munthu
mwini cuma cambiri wa banja la Elimeleki; dzina lace ndiye
Boazi. 2Nati Rute Mmoabu kwa Naomi, Mundilole ndimuke
kumunda, ndikatole khunkha is ngala za tirigu, kumtsata iye
amene adzandikomeramtima. Nanena naye, Muka, mwana
wanga. 3Namuka iye, nakatola khunkha m'munda namatsata
ocekawo; ndipo kudangotero naye kuti deralo la munda linali la
Boazi, ndiye wa banja la Elimeleki. 4Ndipo taona, Boazi anafuma ku
Betelehemu, nati kwa oceka, Yehova akhale nanu. Namyankha iwo,
Yehova akudalitseni. 5Nati Boazi kwa mnyamata wace
woyang'anira ocekawo, Mkazi uyu ngwa yani? 6Ndipo mnyamata
woyang'anira ocekawo anayankha nati, Ndiye mkazi Mmoabuyo
anabwera ndi Naomi ku dziko la Moabu; 7ndipo anati, Undilole,
ndikunkhe ndiole pakati pa mitolo potsata ocekawo; nadza iye
nakhalakhala kuyambira m'mawa mpaka tsopano; koma
m'nyumba samakhalitsamo. 8Pamenepo Boazi ananena ndi Rute,
Ulikumva, mwana wanga? Usakakunkha m'munda mwina, kapena
kupitirira pano, koma uumirire adzakazi anga mommuno. 9Maso
ako akhale pa munda acekawo, ndi kuwatsata; kodi sindinawauza
anyamata asakukhudze? Ndipo ukamva ludzu, muka kumitsuko,
ukamweko otunga anyamatawo, 10Potero anagwa nkhope yace
pansi, nadziweramira pansi, nanena naye, Mwandikomera mtima
cifukwa ninji kuti mundisamalira ine, popeza ndine
mlendo? 11Ndipo Boazi anayankha nanena naye, Anandifotokozera
bwino zonse unacitira mpongozi wako atafa mwamuna wako; ndi
kuti wasiya atate wako ndi mako, ndi dziko lobadwirako iwe, ndi
kudza kwa anthu osawadziwa iwe kale. 12Yehova akubwezere
nchito yako, nakupatse mphotho yokwanira Yehova, Mulungu wa
Israyeli, amene unadza kuthawira pansi pa mapiko ace. 13Nati iye,
Mundikomere mtima mbuye wanga, popeza mwandisangalatsa,
popezanso mwanena cokondweretsa mtima wa mdzakazi wanu,
ndingakhale ine sindine ngati mmodzi wa adzakazi anu. 14Ndipo pa
nthawi ya kudya Boazi ananena naye, Sendera kuno, nudyeko
mkate; nusunse nthongo yako m'vinyo wosasayo. Nakhala iye
m'mbali mwa ocekawo; ndipo anamtambasulira dzanja kumninkha
tirigu wokazinga, nadya iye, nakhuta, nasiyapo. 15Ndipo ataumirira
kukatola khunkha, Boazi analamulira anyamata ace ndi kuti, Atole
khunkha ngakhale pakati pa mitolo, musamcititse
manyazi. 16Ndiponso mumtayire za m'manja, ndi kuzisiya, natole
khunkha, osamdzudzula. 17Natola khunka iye m'munda mpaka
madzulo; naomba khunkhalo napeza ngati licero la
barele, 18nalisenza nalowa kumudzi; ndipo mpongozi wace anaona

khunkhalo; Rute naturutsanso nampatsa mkute uja anausiya atakhuta. 19Ndipo mpongozi wace ananena naye, Unakatola kuti khunkha lero? ndi nchito udaigwira kuti? Adalitsike iye amene anakusamalira. Ndipo anamfotokozera mpongozi wace munthu amene anakagwirako nchito, nati, Dzina lace la munthuyo ndinakagwirako nchito lero ndiye Boazi. 20Nati Naomi kwa mpongozi wace, Yehova amdalitse amene sanaleka kuwacitira zokoma amoyo, ndi akufa. Ndipo Naomi ananena baye, Munthuyu ndiye mbale wathu, ndiye mmodzi wa iwo otiombolera colowa. 21Ndipo Rute Mmoabu anati, Ananenanso nane ndithu, Uwaumirire anyamata anga, mpaka atatha kuceka zanga zonse za m'minda. 22Nati Naomi kwa Rute mpongozi wace, Ncabwino, mwana wanga, kuti uzituruka nao adzakazi ace, ndi kuti asakukomane m'munda wina uti wonse. 23Momwemo anaumirira adzakazi a Boazi kuti atole khunkha kufikira atatha kuceka barele ndi tirigu; ndipo anakhala iye kwao kwa mpongozi wace.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Boazi anena za kumuombolera Rute colowa

1Pamenepo Naomi mpongozi wace ananena naye, Mwana wanga,
kodi ndisakufunire popumulako, kuti ukhale bwino? 2Nanga Boazi
wodziwana nafe, amene unakhala nao adzakazi ace? Taona, usiku
uno apuntha barele popunthirapo. 3Usambe tsono, nudzole,
nubvale zobvala zako, nutsikire popunthirapo, koma usadziwike
naye munthuyo, koma atatha kudya ndi kumwa ndiko. 4Ndipo
kudzali, akagona, upenye apo ati agone, numuke, nubvundukule
ku mapazi ace, nugone, ndi iyeyo adzakufotokozera zoyenera
kucita iwe. 5Ndipo ananena naye, Zonse muzinena
ndidzacita. 6Pamenepo anatsikira popunthirapo, nacita zonse
monga umo mpongozi wace adamuuza. 7Ndipo atatha Boazi kudya
ndi kumwa, nusekerera mtima wace, anakagona kuthungo kwa
mulu wa tirigu; nadza iye kacetecete, nabvuodukula ku mapazi
ace, nagona. 8Ndipo kunali, pakati pa usiku munthuyo
anadzidzimuka, natembenuka; ndipo taona pa mapazi ace pagona
mkazi. 9Nati iye, Ndiwe yani? Nayankha iye, Ndine Rute mdzakazi
wanu; mupfunde mdzakazi wanu copfunda canu, pakuti inu ndinu
wondiombolera colowa. 10Nati iye, Yehova akudalitse, mwana
wanga. Cokoma cako wacicita potsiriza pano, ciposa cakuyamba
cija, popeza sunatsata anyamata, angakhale osauka angakhale
acuma. 11Ndipo tsopano, mwana wanga, usaope; ndidzakucitira
zonse unenazi; pakuti onse a pa mudzi wa anthu a mtundu wanga
adziwa kuti iwe ndiwe mkazi waulemu. 12Tsopano ndipo, zoonadi,
ine ndine wakukuombolera colowa, koma pali wakukuombolera
woposa ine. 13Gona usiku uno, ndipo kudzali m'mawa,
akakuombolera, cabwino, akuombolere; koma ngati safuna
kukuombolera, pali Yehova, ndidzakuombolera colowa ndine; gona
mpaka m'mawa. 14Nagona ku mapazi ace mpaka m'mawa;
nalawira asanazindikirane anthu, Pakuti anati, Cisadziwike kuti
mkaziyo anadza popunthirapo, 15Ndipo anati, Bwera naco
copfunda cako, nucigwire; nacigwira iye; ndipo anayesa miyeso
isanu ndi umodzi ya barele, namsenza; atatero analowa
m'mudzi. 16Ndipo pamene anadza kwa mpongozi wace, iye anati,
Wapeza bwanji, mwana wanga? Pamenepo anamfotokozera zonse
anamcitira munthuyo. 17Natinso, Miyeso iyi isanu ndi umodzi ya
barele anandipatsa, pakuti anati, Usafike kwa mpongozi wako
wopanda kanthu. 18Ndipo anati, Khala ulipo, mwana wanga; mpaka
udziwa umo ukhalire mlandu; pakuti munthuyo sadzauleka mpaka
ataútha mlanduwo lero lino.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Boazi akwatira Rute nabadwa Obedi

1Ndipo Boazi anakwera kumka kucipata, nakhala pansi pomwepo;
ndipo taona, woombolera winayo adanena Boazi analinkupita; nati
iye, Iwe uje, pambuka, khala pansi apa; napambuka iye, nakhala
pansi. 2Ndipo anatenga amuna khumi a akulu a mudzi, nati,
Mukhale pansi apa. Nakhala pansi iwo. 3Pamenepo anati kwa
woombolerayo, Naomi anabwerayo ku dziko la Moabu ati agulitse
kadziko kala kadali ka mbale wathu Elimeleki; 4ndipo ndati
ndikuululira ici, ndi kuti, Ugule aka pamaso pa nzika, ndi pamaso
pa akulu a anthu a kwathu. Ukafuna kuombola ombola; koma
ukapanda kuombola, undiuze, ndidziwe; pakuti palibe woombola
koma iwe, ndi ine pambuyo pako. Pamenepo anati,
Ndidzaombola. 5Nati Boazi, Tsiku lomwelo ugula mundawo pa
dzanja la Naomi, uugulanso kwa Rute, Mmoabu, mkazi wa
wakufayo, kuukitsira dzina la wakufayo pa colowa cace. 6Ndipo
woombolerayo anati, Sindikhoza kuuombola kwa ine ndekha,
ndingaononge colowa canga; udzitengere wekha mphamvu yanga
yakuombola; popeza sinditha kuombola. 7Koma kale m'Israyeli
pakuombola ndi pakusinthana, kutsimikiza mlandu wonse, akatero:
munthu abvula nsapato yace, naipereka kwa mnansi wace; ndiwo
matsimikizidwe m'Israyeli. 8Ndipo woombolayo anati kwa Boazi,
Udzigulire wekha kadzikoko. Nabvula nsapato yace. 9Nati Boazi
kwa akulu, ndi kwa anthu onse, Inu ndinu mboni lero lino kuti
ndagula zonse za Elimeleki, ndi zonse za Kilioni, ndi Maloni, pa
dzanja la Naomi. 10Ndiponso Rute Mmoabu, mkazi wa Maloni
ndamgula akhale mkazi wanga kuukitsa dzina la wakufayo pa
colowa cace; kuti dzina la wakufayo lisaiwalike pakati pa abale ace,
ndi pa cipata ca malo ace; inu ndinu mboni lero lino. 11Pamenepo
anthu onse anali kucipata, ndi akuru, anati, Tiri mboni ife. Yehova
acite kuti mkazi wakulowayo m'nyumba mwako ange Rakele ndi
Leya, amene anamanga nyumba ya Israyeli, iwo awiri; nucite iwe
moyenera m'Efrata, numveke m'Betelehemu; 12ndi nyumba yako
inge nyumba ya Perezi, amene Tamare anambalira Yuda, ndi mbeu
imene Yehova adzakupatsa ya namwali uyu. 13Momwemo Boazi
anatenga Rute, nakhala iye mkazi wace; ndipo analowa kwa iye;
nalola Yehova kuti aime, ndipo anabala mwana
wamwamuna. 14Pamenepo akazi anati kwa Naomi, Adalitsike
Yehova amene sana lola kuti akusowe woombolera lero; nilimveke
dzina lace m'Israyeli, 15Nakhale uyu wakukubwezera moyo, ndi
wodyetsa ukalamba wako; pakuti mpongozi wako amene
akukonda, amene aposa ana amuna asanu ndi awiri kukuthandiza,
anambala. 16Ndipo Naomi anamtenga mwanayo, namuika
pacifuwa pace, nakhala mlezi wace. 17Ndi akazi anansi ace

anamucha dzina, ndi kuti, Kwa Naomi kwambadwira mwana;
namucha dzina lace Ohedi; ndiye atate wa Jese atate wa Davide.
18Iyo ndiyo mibadwo ya Perezi; Perezi anabala Hezironi; 19ndi
Hezironi anabala Ramu, ndi Ramu anabala Aminadabu; 20ndi
Aminadabu anabala Nasoni, ndi Nasoni anabala Salimoni; 21ndi
Salimoni anabala Boazi, ndi Boazi anabala Obedi; 22ndi Obedi
anabala Jese, ndi Jese anabala Davide.

©The Bible Society of Malawi, 1992

1 Samuel

1 Samueli 1

1NDIPO panali munthu wina wa ku Ramatayimu Zofimu, wa dziko la mapiri la Efraimu, dzina lace ndiye Elikana, mwana wace wa Yerohamu, mwana wa Elihu, mwana wa Tohu, mwana wa Zufu, M-efraimu. 2Iyeyu anali nao akazi awiri; winayo dzina lace ndi Hana, mnzace dzina lace ndi Penina. Ndipo Penina anaona ana, koma Hana anali wouma. 3Ndipo munthuyu akakwera caka ndi caka kuturuka m'mudzi mwace kukalambira ndi kupereka nsembe kwa Mulungu wa makamu m'Silo. Ndipo pomwepo panali ana amuna awiri a Eli, ansembe a Yehova, ndiwo Hofeni ndi Pinehasi. 4Ndipo pofika tsiku lakuti Elikana akapereka nsembe, iye anapatsa Penina mkazi wace, ndi ana ace onse, amuna ndi akazi, gawo lao; 5koma anapatsa Hana magawo awiri, cifukwa anakonda Hana, koma Mulungu anatseka mimba yace. 6Ndipo womnyodolayo anamputa kwakukuru, kuti amuwawitse mtima, popeza Yehova anatseka mimba yace. 7Ndipo popeza munthuyo adatero caka ndi caka, popita mkaziyo ku nyumba ya Yehova, mnzaceyo amamputa; cifukwa cace iye analira misozi, nakana kudya. 8Ndipo mwamuna wace Elikana anati kwa iye, Hana, umaliriranji? ndipo umakaniranji kudya? ndipo mtima wako uwawa ninji? Ine sindiri wakuposa ana khumi kwa iwe kodi? 9Comweco Hana anauka atadya m'Silo, ndi kumwa. Ndipo Eli wansembeyo anakhala pa mpando wace pa mphuthu ya Kacisi wa Yehova. 10Ndipo mkaziyo anali ndi mtima wowawa, napemphera kwa Yehova, naliratu misozi; 11nalonjeza cowinda, nati, Yehova wa makamu, mukapenyera ndithu kusauka kwa mdzakazi wanu, ndi kukumbukila ine, ndi kusaiwala mdzakazi wanu, mukapatsa mdzakazi wanu mwana wamwamuna, ine ndidzampereka kwa Yehova masiku onse a moyo wace, ndipo palibe lumo lidzapita pamutu pace. 12Ndipo panali, m'mene iye analikupempherabe pamaso pa Yehova, Eli anapenyerera pakamwa pace. 13Koma Hana ananena mu mtima; milomo yace inatukula, koma mau ace sanamveka; cifukwa cace Eli anamuyesa woledzera. 14Ndipo Eli anati kwa iye, Udzaleka liti kuledzera? cotsa vinyo wako. 15Ndipo Hana anayankha, nati, Iai, mbuyanga. Ine ndiri mkazi wa mtima wacisoni; sindinamwa vinyo kapena cakumwa cowawa, koma ndinatsanulira mtima wanga pamaso pa Yehova. 16Musamandiyesa mdzakazi wanu mkazi woipa; cifukwa kufikira lero ndinalankhula mwa kucuruka kwa kudandaula kwanga ndi kubvutika kwanga. 17Pamenepo Eli anayankha nati, Pita ndi mtendere; ndipo Mulungu wa Israyeli akupatse copempha cako unacipempha, kwa iye. 18Ndipo iye anati, Mumkomere mtima mdzakazi wanu. Comweco mkaziyo anamuka, nakadya, ndi nkhope

yace siinakhalanso yacisoni. 19Ndipo iwo anauka mamawa,
nalambira pamaso pa Yehova, nabwerera, nafikanso kwao ku Rama;
ndipo Elikana anadziwa mkazi wace Hana, Yehova namkumbukila
iye. 20Ndipo panali pamene nthawi yace inafika, Hana anaima,
nabala mwana wamwamuna: namucha dzina lace Samueli, nati,
Cifukwa ndinampempha kwa Yehova, 21Ndipo munthuyo Elikana, ndi
a pa banja lace onse, anakwera kukapereka kwa Yehova nsembe ya
caka ndi caka, ndi ya cowinda cace. 22Koma Hana sadakwera,
cifukwa kuti anati kwa mwamuna wace, Sindidzakwerako kufikira
mwanayo ataleka kuyamwa, pamenepo ndidzapita naye kuti aoneke
pamaso pa Yehova, ndi kukhalako cikhalire. 23Ndipo Elikana
mwamuna wace anati, Cita cimene cikukomera nukhale kufikira
utamletsa kuyamwa; komatu Yehova akhazikitse mau ace.
Comweco mkaziyo anakhala nayamwitsa mwana wace, kufikira
anamletsa kuyamwa. 24Ndipo atamletsa kuyamwa anakwera naye,
pamodzi ndi ng'ombe ya zaka zitatu, ndi efa wa ufa, ndi thumba la
vinyo, nafika naye ku nyumba ya Yehova ku Silo; koma mwanayo
anali wamng'ono. 25Ndipo iwo anapha ng'ombe, nabwera naye
mwanayo kwa Eli. 26Ndipo mkaziyo ananena, Mbuye wanga, pali
moyo wanu, zoonadi ine ndine mkazi uja ndidaima pano ndi inu, ndi
kupemphera kwa Yehova. 27Ndinampempha mwanayu; ndipo
Yehova anandipatsa copemphacanga ndinacipempha kwa
iye; 28cifukwa cace inenso ndinampereka kwa Yehova; masiku onse
a moyo wace aperekedwa kwa Yehova. Ndipo analambira Yehova
pomwepo.
©The Bible Society of Malawi, 1992

Coyamikira ca Hana

1 Ndipo Hana anapemphera, nati
Mtima wanga umyuka mokondwera kwa Yehova,
Nyanga yanga yakwezeka mwa Yehova;
Pakamwa panga pakula kwa adani anga;
Popeza ndikondwera m'cipulumutsocanu.
2 Palibe wina woyera ngati Yehova;
Palibe wina koma Inu nokha;
Palibenso thanthwe longa Mulungu wathu.
3 Musalankhulenso modzikuza kwambiri motero;
M'kamwa mwanu musaturuke zolulutsa;
Cifukwa Yehova ali Mulungu wanzeru,
Ndipo iye ayesa zocita anthu.
4 Mauta a amphamvu anathyoka,
Koma okhumudwawo amangiridwa ndi mphamvu m'cuuno.
5 Amene anakhuta anakasuma cakudya;
Koma anjalawo anacira;
Inde cumba cabala asanu ndi awiri:
Ndipo iye amene ali ndi ana ambiri acita liwondewonde.
6 Yehova amapha, napatsa moyo:
Iye amatsitsa kumanda, naukitsanso.
7 Yehova asaukitsa, nalemeza;
Acepetsa, nakuzanso.
8 Amuutsa waumphawi m'pfumbi,
Nanyamula wosowa padzala,
Kukamkhalitsa kwa akalonga;
Ndi kuti akhale naco colowa ca cimpando ca ulemerero;
Cifukwa nsanamira za dziko lapansi nza Yehova,
Ndipo iye anakhazika dziko pa izo,
9 Adzasunga mapazi a okoodedwaace,
Koma oipawo adzawakhalitsa cete mumdima;
Pakuti palibe munthu adzapambana ndi mphamvu,
10 Otsutsana ndi Yehova adzaphwanyika;
Kumwamba iye adzagunda pa iwo:
Yehova adzaweruza malekezero a dziko:
Ndipo adzapatsa mphamvu mfumuyace,
Nadzakweza nyanga ya wodzozedwa wace.
11 Ndipo Elikana anauka kwao ku Rama, mwanayo natumikira Yehova pamaso pa Eli wansembeyo.

Kucimwa kwa ana a Eli

12 Koma ana a Eli anali oipa; sanadziwa Yehova. 13 Ndipo macitidwe a ansembe akucitira anthu ndiwo, kuti pamene munthu ali yense akapereka nsembe, mnyamata wa wansembeyo akabwera, nyama

iri ciwirire, ndi cobvuulira ca ngowe ca mana atatu m'dzanja
lace; 14nacipisa m'cimphuli, kapena mumkhate, kapena m'nkhali,
kapena mumphika; yonse imene cobvuuliraco cinaiturutsa,
wansembeyo anaitenga ikhale yace. Adafotero ku Silo ndi Aisrayeli
onse akufika kumeneko. 15Ngakhale asanayambe kupsereza
mafuta, amadza mnyamata wa wansembe, namuuza wopereka
nsembe, nati, Umpatse wansembeyo nyama yoti akaoce; pakuti
safuna nyama yako yophika koma yaiwisi. 16Ndipo ngati munthu
akanena naye, Koma adzatentha mafuta tsopano apa, atatha,
utenge monga mtima wako ufuna; uyo akanena naye, lai, koma
undipatsire iyo tsopanoli, ukapanda kutero ndidzailanda. 17Ndipo
zoipa za anyamatawo zinali zazikuru ndithu pamaso pa Yehova;
pakuti anthu anaipidwa ndi nsembe ya Yehova. 18Koma Samueli
anatumikira pamaso pa Yehova akali mwana, atamangira m'cuuno
ndi efodi wabafuta. 19Ndiponso amace akamsokera mwinjiro
waung'ono, nabwera nao kwa iye caka ndi caka, pakudza pamodzi
ndi mwamuna wace kudzapereka nsembe ya pacaka. 20Ndipo Eli
anadalitsa Elikana ndi mkazi wace, nati, Yehova akupatse mbeu ndi
mkazi uyu m'malo mwa iye amene munampempha kwa Yehova.
Ndipo iwowa anabwera kwao. 21Ndipo Yehova anakumbukila Hana,
naima iye, nabala ana amuna atatu, ndi ana akazi awiri. Ndipo
mwanayo Samueli anakula pamaso pa Yehova.
22Ndipo Eli anali wokalamba ndithu; namva zonse ana ace
anacitira Aisrayeli onse, ndi kuti anagona ndi akazi akusonkhana
pa khomo la cihema cokomanako. 23Ndipo iye ananena nao,
Mumacitiranji zotere? popeza ndirinkumva za macitidwe anu oipa
kwa anthu onsewa. 24lai, ana anga, popeza mbiri imene
ndirikuimva siri yabwino iai; mulikulakwitsa anthu a
Yehova. 25Munthu akacimwira munthu mnzace oweruza
adzaweruza mrandu wace; koma ngati munthu acimwira Yehova,
adzampembedzera ndani? Koma ngakhale adatero, iwo aja
anakhalabe osamvera mau a atate wao, cifukwa Yehova adati
adzawaononga. 26Ndipo mwanayo Samueli anakulakula, ndipo
Yehova ndi anthu omwe anamkomera mtima.

Mneneri aneneratu za kupasuka kwa banja la Eli

27Ndipo anafika kwa Eli munthu wa Mulungu, nanena naye, Atero
Yehova, Kodi Ine ndinadziulula kwa banja la kholo lako, muja anali
m'Aigupto, m'nyumba ya Farao? 28Kodi sindinasankhula iye pakati
pa mafuko onse a Israyeli, akhale wansembe wanga, kuti apereke
nsembe pa guwa langa, nafukize zonunkhira, nabvale efodi
pamaso panga? Kodi sindinapatsa banja la kholo lako zopereka
zonse za kumoto za ana a Israyeli? 29Nanga umaponnderezeranji
nsembe yanga ndi copereka canga, zimene ndinalamulira
m'mokhalamo mwanga; ndipo ucitira ana ako ulemu koposa Ine,

kudzinenepetsa inu nokha ndi zokometsetsa za zopereka zao
zonse za Aisrayeli, anthu anga? 30Cifukwa cace Yehova Mulungu
wa Israyeli akuti, Ndinaterodi kuti banja lako ndi banja la kholo lako
lidzayenda pamaso panga nthawi zonse; koma tsopano Yehova ati,
Cikhale kutali ndi Ine; popeza amene andilemekeza Ine, Inenso
ndidzawalemekeza iwowa, ndipo akundipeputsa Ine,
adzapeputsidwa. 31Ona, masiku alinkudza amene ndidzadula
dzanja lako, ndi dzanja la nyumba ya kholo lako, kuti m'banja lako
musakhalenso nkhalamba, 32Ndipo udzaona masautso a
mokhalamo Mulungu, m'malo mwa zabwino zonse iye akadacitira
Israyeli. Banja lako lidzakhala opanda nkhalamba cikhalire. 33Ndipo
munthu wako, amene ndidzamleka osamlikha pa guwa langa,
adzatha maso ako, ndi kumvetsa mtima wako cisoni; ndipo obadwa
onse a m'banja lako adzamwalira akali biriwiri. 34Ndipo ici cimene
cidzafikira ana ako awiri Hofeni ndi Pinehasi, cidzakhala cizindikilo
kwa iwo, tsiku limodzi adzafa iwo onse awiri. 35Ndipo
ndidzadziukitsira wansembe wokhulupirika, amene adzacita
monga cimene ciri mumtima mwanga ndi m'cifuniro canga; ndipo
ndidzammangira nyumba yokhazikika, ndipo iyeyu adzayenda
pamaso pa wodzozedwa wanga masiku onse. 36Ndipo kudzali kuti
yense wakusiyidwa wa m'banja lako adzabwera kwa iye
nadzawerama ndi kupempha ndalama ndi cakudya, nadzati,
Mundipatsetu nchito yina ya wansembe, kuti ndikaona kakudya.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masomphenya a Samueli

1Ndipo mwanayo Samueli anatumikira Yehova pamaso pa Eli.
Ndipo masiku aja mau a Yehova anamveka kamodzi kamodzi;
masomphenya sanaoneka-oneka. 2Ndipo kunali nthawi yomweyo
Eli atagona m'malo mwace (maso ace anayamba cizirezire osatha
kupenya bwino); 3ndi nyali ya Mulungu isanazime, Samueli nagona
m'Kacisi wa Yehova, m'mene munali likasa la Mulungu. 4Pamenepo
Yehova anaitana Samueli; ndipo iye anayankha kuti, Ndiri
pano. 5Ndipo anathamangira kwa Eli nati, Ndine, popeza
mwandiitana ine. Ndipo iye anati, Sindinaitana, kagone. Napita iye,
nagona, 6Ndipo Yehova anabwereza kumuitana, ndi kuti, Samueli.
Ndipo Samueli anauka, napita kwa Eli, nati, Ndine, pakuti
mwandiitana ndithu. Koma iye anayankha, Sindinaitana, mwana
wanga; kagone. 7Koma Samueli sanadziwe Yehova, ndiponso mau
a Yehova sanaululidwe kwa iye. 8Ndipo Yehova anabwereza
kumuitana Samueli nthawi yacitatu. Ndipo iye anauka napita kwa
Eli, nati, Ndine, pakuti mwandiitana ndithu. Ndipo Eli anazindikira
kuti ndiye Yehova amene analikuitana mwanayo. 9Cifukwa cace Eli
anati kwa Samueli, Pita, ukagone; ndipo akakuitananso,
ukabvomere, kuti, Nenani, Yehova, popeza mnyamata wanu
akumva. Comweco Samueli anakagona m'malo mwace. 10Ndipo
Yehova anabwera, naimapo, namuitana monga momwemo,
Samueli, Samueli. Pompo Samueli anayankha, Nenani, popeza
mnyamata wanu akumva. 11Ndipo Yehova ananena ndi Samueli,
Taona, ndidzacita mwa Israyeli coliritsa mwini khutu kwa munthu
yense wakucimva. 12Tsiku lija udidzamcitira Eli zonse
ndinaneneratu za pa banja lace, kuciyamba ndi
kucitsiriza. 13Popeza ndinamuuza kuti ndidzaweruza nyumba yace
kosatha cifukwa ca zoipa anazidziwa, popeza ana ace
anadzitengera temberero, koma iye sanawaletsa. 14Cifukwa cace
ndinalumbira kwa banja la Eli, kuti zoipa za banja la Elilo
sizidzafafanizidwa ndi nsembe, kapena ndi zopereka, ku nthawi
zonse.

Samueli aulula kwa Eli

15Ndipo Samueli anagona kufikira m'mawa, natsegula zitseko za
nyumba ya Yehova. Ndipo Samueli anaopa kudziwitsa Eli
masomphenyawo. 16Pamenepo Eli anaitana Samueli, nati, Mwana
wanga, Samueli. Nati iye, Ndine. 17Ndipo anati, Anakuuza cinthu
canji? Usandibisire ine. Mulungu akulangendi kuonjezapo, ngati
undibisira cimodzi ca zonse zija adanena nawe. 18Ndipo Samueli
anamuuza zonse, sanambisira kanthu. Ndipo iye anati, Ndiye
Yehova; acite comkomera pamaso pace.

19Ndipo Samueli anakula, Yehova nakhala naye, osalola kuti mau
ace amodzi apite pacabe. 20Ndipo Aisrayeli onse, kuyambira ku
Dani kufikira ku Beereseba anazindikira kuti Samueli anakhazikika
akhale mneneri wa Yehova. 21Ndipo Yehova anaonekanso m'Silo,
pakuti Yehova anadziulula kwa Samueli ku Silo, mwa mau a
Yehova.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Afilisti akantha Aisrayeli

1Ndipo mau a Samueli anafikira kwa Aisrayeli onse. Ndipo Aisrayeli
anaturuka kukaponyana nkhondo ndi Afilisti, namanga zithando
zao ku Ebenezeri; Afilistiwo namanga m'Afeki. 2Ndipo Afilistiwo
anandandalitsa nkhondo yao pa Aisrayeli; ndipo pokomana
nkhondo Aisrayeli anakanthidwa ndi Afilisti. Ndipo anapha
kuthengoko anthu zikwi zinai a khamu lao.

Likasa lilandidwa, Hofeni ndi Pinehasi aphedwa

3Ndipo pamene anthu anafika ku zithandozo, akuru a Israyeli anati,
Yehova anatikanthiranji lero pamaso pa Afilisti? Tikadzitengere
likasa la cipangano la Yehova ku Silo, kuti likabwera pakati pa ife,
lidzatipulumutsa m'dzanja la adani athu. 4Cifukwa cace anatumiza
ku Silo kuti akatenge kumeneko likasalo la cipangano la Yehova wa
makamu, wokhala pakati pa akerubi; ndipo ana awiriwo a Eli,
Hofeni ndi Pinehasi anali komweko ndi likasa la cipangano la
Yehova. 5Pakufika likasalo la cipangano la Yehova kuzithando,
Aisrayeli onse anapfuula ndi mau okweza, kotero kuti dziko linacita
cibvomezi. 6Ndipo Afilistiwo pakumva kubuma pa kupfuula kwao,
anati, Phokoso ili la kupfuula kwakukuru ku zithando za Aisrayeli
litani? Ndipo anamva kuti likasa la Yehova lidzafika ku
zithandozo. 7Ndipo Afilisti anaopa, pakuti anati, Mulungu wafika
kuzithando. Ndipo iwo anati, Tsoka kwa ife! popeza kale lonse
panalibe cinthu cotere. 8Tsoka kwa ife! adzatilanditsa ndani
m'manja a milungu yamphamvu imeneyi? Milungu ija inakantha
Aaigupto ndi masautso onse m'cipululu ndi yomweyi. 9Limbikani,
ndipo mucite camuna, Afilisti inu, kuti mungakhale akapolo a
Ahebri, monga iwowa anali akapolo anu. Citani camuna
nimuponyane nao. 10Ndipo Afilisti anaponyana nao, nakantha
Aisrayeli; iwowa nathawira, munthu yense ku hema wace; ndipo
kunali kuwapha kwakukuru; popeza anafako Aisrayeli zikwi makumi
atatu a oyenda pansi. 11Ndipo likasa la Mulungu linalandidwa, ndi
ana awiri a Eli, Hofeni ndi Pinehasi, anaphedwa. 12Ndipo munthu
wa pfuko la Benjamini anathamanga kucokera ku khamu la
ankhondo, nafika ku Silo tsiku lomwelo, ndi zobvala zace
zong'ambika, ndi dothi pamutu pace.

Imfa ya Eli

13Pakufika iye, onani, Eli analikukhala pampando m'mbali mwa
njira, alikuyang'anira, popeza mtima wace unanthunthumira
cifukwa ca likasa la Mulungu, Pamene munthu uja anafika
m'mudzimo, nanena izi, a m'mudzi monse analira. 14Ndipo Eli,
pakumva kubuma kwa kulira kwao, anati, Alikupokoseranji? Ndipo
munthuyo anafulumira, nadza nauza Eli. 15Koma Eli anali ndi zaka
makumi asanu ndi anai kudza zisanu ndi zitatu; ndipo maso ace

anangokhala tong'o osapenya, 16Ndipo munthuyo anati kwa Eli, Ine ndine amene ndacokera ku khamu la ankhondo, ndipo ndathawa lero ku khamu la ankhondo. Ndipo iye anati, a Nkhondoyo idatani, mwana wanga? 17Ndipo wakubwera ndi mauyo anayankha, nati, Israyeli anathawa pamaso pa Afilisti, ndiponso kunali kuwapha kwakukuru kwa anthu, ndi ana anu awiri omwe Hofeni ndi Pinehasi afa, ndipo likasa la Mulungu lalandiwa. 18Ndipo kunali, pakunena za likasa la Mulungu, iye anagwa cambuyo pa mpando wace pam bali pa cipata, ndi khosi lace linathyoka, nafa iye; popeza anali wokalamba ndi wamkuru thupi. Ndipo adaweruza anthu a Israyeli zaka makumi anai. 19Ndipo mpongozi wace, mkazi wa Pinehasi, anali ndi mimba, pafupi pa nthawi yace yakuona mwana; ndipo pakumva iye mau akuti likasa la Mulungu linalandidwa, ndi kuti mpongozi wace, ndi mwamuna wace anafa, iyeyu anawerama, nabala mwana; popeza kucira kwace kwamdzera. 20Ndipo pamene adati amwalire, anthu akazi akukhala naye ananena, Usaope, popeza waona mwana wamwamuna. Koma iye sanayankha, kapena kusamalira. 21Ndipo iye anamucha dzina la mwanayo Ikabodi, nati, Ulemerero wacoka kwa Israyeli; cifukwa likasa la Mulungu linalandidwa, ndi cifukwa ca mpongozi wace ndi mwamuna wace. 22Ndipo iye anati, Ulemerero wacoka kwa Israyeli; cifukwa likasa la Mulungu lalandidwa.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Likasa la Mulungu ku nyumba ya Dagoni

1Ndipo Afilisti anatenga likasa la Mulungu, nacoka nalo ku
Ebenezeri, napita ku Asidodi. 2Ndipo Afilistiwo anatenga likasa la
Mulungu, nafika nalo ku nyumba ya Dagoni, naliika pafupi ndi
Dagoni. 3Ndipo pakuuka a ku Asidodi mamawa, taonani Dagoni
adagwa pansi, nagona cafufumimba patsogolo pa likasa la Yehova.
Ndipo iwo anatenga Dagoni namuimikanso m'malo mwace. 4Ndipo
m'mawa mwace polawirira, taonani, Dagoni adagwa pansi, nagona
cafufumimba patsogolo pa likasa la Yehova; ndipo mutu wace ndi
zikhato zonse ziwiri za manja ace zinagona zoduka paciundo;
Dagoni anatsala thupi lokha. 5Cifukwa cace angakhale ansembe,
angakhale ena akulowa m'nyumba ya Dagoni, palibe woponda pa
ciundo ca Dagoni ku Asidodi, kufikira lero lino.

Masauko a Afilisti cifukwa ca likasa

6Koma Yehova anabvuta iwo a ku Asidodi ndi dzanja lace,
nawaononga, nawazunza ndi mafundo, m'Asidodi ndi m'miraga
yace. 7Ndipo pamene anthu a ku Asidodi anaona kuti ncomweco,
anati iwowa, Likasa la Mulungu wa Israyeli lisakhalitse ndi ife;
popeza dzanja lace litiwawira ife, ndi Dagoni mulungu
wathu. 8Cifukwa cace anatumiza mithenga, nasonkhanitsa
mafumu onse a Afilisti, nati, Ticite nalo ciani likasa la Mulungu wa
Israyeli? Ndipo anati, Anyamule likasa la Mulungu kunka nalo ku
Gati, Ndipo ananyamula likasalo la Mulungu wa Israyeli, napita
nalo kumeneko. 9Ndipo kunali atafika nalo, dzanja la Yehova
linatsutsa mudziwo ndi kusautsa kwakukuru; ndipo anazunza anthu
a mudziwo, akuru ndi ang'ono; ndi mafundo anawabuka. 10Cifukwa
cace anatumiza likasa la Mulungu ku Ekroni. Ndipo kunali pofika
likasalo ku Ekroni, a ku Ekroni anapfuula nati, Anadzatitulira likasa
la Mulungu wa Israyeli, kutipha ife ndi ana athu. 11Cifukwa cace
anatumiza, nasonkhanitsa mafumu onse a Afilisti, ndipo iwowa
anati, Cotsani likasa la Mulungu wa Israyeli, lipitenso kumalo
kwace, kuti lingationonge ife, ndi anthu athu; pakuti kunali
kusautsa koopsa m'mudzi monse; dzanja la Mulungu linabvutadi
pamenepo. 12Ndipo amene anapanda kufa anagwidwa ndi
mafundowo; ndi kulira kwa mudziwo kunakwera kumwamba.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Afilisti abweza likasa ku dziko la Aisrayeli

1Ndipo likasa la Yehova linakhala ku dziko la Afilisti miyezi isanu
ndi iwiri. 2Ndipo Afilistiwo anaitana ansembe ndi oombeza, nati,
Ticitenji ndi likasa la Yehova? mutidziwitse cimene tilitumize naco
kumalo kwace. 3Ndipo iwo anati, Ngati mulitumiza kwina likasa la
Mulungu wa Israyeli, musalitumize lopanda kanthu; koma
makamaka mulibweze ndi nsembe yoparamula, mukatero
mudzaciritsidwa, ndi kudziwa cifukwa cace dzanja lace liri pa inu
losacoka. 4Ndipo iwo aja anati, Tidzambwezera nsembe
yoparamula yanji? Ndipo iwo anati, Mafundo asanu agolidi, ndi
mbewa zisanu zagolidi, monga mwa ciwerengo ca mafumu a
Afilisti; popeza kusauka kumodzi kunali pa inu nonse, ndi pa
mafumu anu. 5Cifukwa cace muzipanga zifanizo za mafundo anu,
ndi zifanizo za mbewa zanu zimene ziipitsa dziko; ndipo mucitire
ulemu Mulungu wa Israyeli; kuti kapena adzaleza dzanja lace pa
inu, ndi pa milungu yanu, ndi pa dziko lanu. 6Mulikuumitsiranji
mitima yanu, monga Aaigupto ndi Farao anaumitsa mitima yao?
Kodi iwo sana lola anthuwo amuke, iye atacita kodabwitsa pakati
pao, ndipo anamuka? 7Cifukwa cace tsono, tengani, nimukonze
gareta latsopano, ndi ng'ombe ziwiri zamkaka, zosalawa goli
cikhalire, ndipo mumange ng'ombezo pagareta, muzicotsere ana
ao kunka nao kwanu; 8ndipo mutenge likasa la Yehova, nimuliike
pagaretapo; nimuike zokometsera zagolidi, zimene muzipereka
kwa iye ngati nsembe yoparamula, m'bokosi pam bali pace;
nimulitumize licoke. 9Ndipo muyang'anire, ngati likwera pa njira ya
malire ace ace ku Betisemesi, iye anaticitira coipa ici cacikuru;
koma likapanda kutero, tidzadziwapo kuti dzanja limene
linatikantha, siliri lace; langotigwera tsokali. 10Ndipo anthuwo
anatero; natenga ng'ombe ziwiri zamkaka, nazimanga pagareta,
natsekera anao kwao; 11naika likasa la Yehova pagaretapo, ndi
bokosi m'mene munali mbewa zagolidi ndi zifanizo za mafundo
ao. 12Ndipo ng'ombezo zinatsata njira yolunjika ku Betisemesi,
niziyenda mumseu, zirikulira poyenda; sizinapambukira ku dzanja
lamanja, kapena kulamanzere; ndipo mafumu a Afilisti anazitsatira
kufikira ku malire a Betisemesi. 13Ndipo a ku Betisemesi
analikumweta tirigu wao m'cigwamo; natukula maso ao, naona
likasalo, nakondwerapakuliona. 14Ndipo garetalo linafika m'munda
wa Yoswa wa ku Betisemesi, ndi kuima momwemo, pa mwala
waukuru; ndipo anawaza matabwa a garetalo, nazipereka
ng'ombezo nsembe yopsereza kwa Yehova. 15Ndipo Alevi anatsitsa
likasa la Yehova, ndi bokosi linali nalo, m'mene munali
zokometsera zagolidi, naziika pa mwala waukuruwo; ndipo anthu a
ku Betisemesi anapereka nsembe zopsereza, naphera nsembe kwa

Yehova tsiku lomwelo. 16Ndipo pamene mafumu asanu a Afilisti
anaonerako, anabwerera kunka ku Ekroni tsiku lomwelo.
17Ndipo amenewa ndiwo mafundo agolidi amene anabwezera kwa
Yehova akhale nsembe yoparamula, kwa Asidodi limodzi, kwa Gaza
limodzi, kwa Asikeloni limodzi, kwa Gati limodzi, kwa Ekroni
limodzi; 18ndiponso mbewa zagolidi, monga ciwerengo ca midzi
yonse ya mafumu asanu a Afilisti, midzi ya malinga, ndi midzi ya
kumiraga; kufikira ku mwala waukuru, adaikapo likasa la Yehova;
mwalawo ulipobe kufikira lero m'munda wa Yoswa wa ku
Betisemesi. 19Ndipo Mulungu anakantha anthu a ku Betisemesi,
cifukwa anasuzumira m'likasa la Yehova, anakantha anthu zikwi
makumi asanu; ndipo anthu analira maliro, cifukwa Yehova
anawakantha anthuwo ndi makanthidwe akuru.

Likasa lisungidwa ku Kiriati-yearimu

20Ndipo a ku Betisemesi anati, Akhoza ndani kuima pamaso pa
Yehova, Mulungu Woyera uyu? Ndipo adzakwera kwa yani
pakuticokera ife? 21Ndipo anatumiza mithenga kwa anthu a ku
Kiriati-yearimu, nati, Afilisti anabwera nalo likasa la Yehova,
mutsike; ndi kukwera nalo kwanu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

1Ndipo anthu a ku Kiriati-yearimu anabwera, natenga likasa la
Yehova, nafika nalo m'nyumba ya Abinadabu paphiri; napatula
mwana wace wamwamuna Eleazeri kuti asunge likasa la Yehova.
Afilisti akanthidwa ku Mizipa
2Ndipo kunali, kuti likasalo linakhala nthawi yaikuru m'Kiriati-
yearimu; popeza linakhalako zaka makumi awiri; ndipo banja lonse
la Israyeli linalirira Yehova. 3Ndipo Samueli analankhula ndi banja
lonse la Israyeli nati, Ngati mukuti mubwerere kunka kwa Yehova
ndi mitima yanu yonse, cotsani pakati pa inu milungu yacilendo,
ndi Asitaroti, nimukonzere Yehova mitima yanu, ndi kumtumikira
iye yekha; mukatero, iye adzakupulumutsani m'manja a
Afilisti. 4Pomwepo ana a Israyeli anacotsa. Abaala ndi Asitaroti,
natumikira Yehova yekha.
5Ndipo Samueli anati, Musonkhanitse Aisrayeli onse ku Mizipa,
ndipo ine ndidzakupempherera kwa Yehova. 6Ndipo anaunjikana
ku Mizipa, natunga madzi, nawatsanula pamaso pa Yehova, nasala
cakudya tsiku lija, nati, Tinacimwira Yehova. Ndipo Samueli
anaweruza ana a Israyeli m'Mizipa. 7Ndipo pamene Afilisti anamva
kuti Aisrayeli anasonkhana pamodzi ku Mizipa, mafumu a Afilisti
anakwera kukayambana ndi Aisrayeli. Ndipo Aisrayeli pakumva ici,
anacita mantha ndi Afilistiwo. 8Ndipo ana a Israyeli anati kwa
Samueli, Musaleke kutipempherera kwa Yehova Mulungu wathu,
kuti iye atipulumutse m'manja a Afilistiwo. 9Ndipo Samueli
anatenga mwana wa nkhosa woyamwa, nampereka wathunthu
kwa Yehova, nsembe yopsereza; ndipo Samueli anapempherera
Israyeli kwa Yehova; ndipo Yehova anambvomereza. 10Ndipo
pamene Samueli analikupereka nsembe yopserezayo, Afilisti
anayandikira kuti aponyane ndi Aisrayeli; koma tsiku lomwe lija
Yehova anagunda ndi kugunda kwakukuru pa Afilistiwo,
nawapolonganitsa. Ndipo anakanthidwa pamaso pa
Aisrayeli. 11Ndipo Aisrayeli anaturuka ku Mizipa, nathamangira
Afilisti, nawakantha mpaka anafika pansi pa Betikara. 12Pamenepo
Samueli anatenga mwala nauimika pakati pa Mizipa ndi Seni,
naucha dzina lace. Ebenezeri, nati, Kufikira pano
Yehovaanatithandiza. 13Comweco anagonjetsa Afilisti, ndino iwo
sanatumphanso malire a Israyeli ndipo dzanja la Yehova linasautsa
Afilisti masiku onse a Samueli. 14Ndipo midzi ya Israyeli imene
Afilisti adailanda kale inabwezedwa kwa Aisrayeli, kuyambira ku
Ekroni kufikira ku Gati; ndi Aisrayeli analanditsa miraga yao
m'manja a Afilisti. Ndipo pakati pa Aisrayeli ndi Aamori panali
mtendere; 15ndipo Samueli anaweruza Israyeli masiku onse a
moyo wace. 16Ndipo anayenda cozungulira caka ndi caka ku Beteli,
ndi ku Giligala, ndi ku Mizipa; naweruza Israyeli m'malo onse

amenewa. 17Ndipo anabwera ku Rama, pakuti nyumba yace inali
kumeneko; ndipo pamenepo anaweruza Israyeli; namangapo guwa
la nsembe la Yehova.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Aisrayeli akhumba mfumu

1Ndipo kunali, pamene Samueli anakalamba, anaika ana ace
amuna akhale oweruza a Israyeli. 2Dzina la mwana wace woyamba
ndiye Yoeli, ndi dzina la waciwiri ndiye Abiya; ndiwo oweruza a ku
Beereseba. 3Ndipo ana ace sanatsanza makhalidwe ace, koma
anapambukira ku cisiriro, nalandira cokometsera mlandu, naipitsa
kuweruza.
4Pamenepo akuru onse a Israyeli anasonkhana, nadza kwa Samueli
ku Rama; 5nanena naye, Taonani, mwakalamba, ndipo ana anu
satsanza makhalidwe anu; tsono, mutilongere mfumu kuti
ikatiweruze, monga umo mucitidwa m'mitundu yonse ya
anthu. 6Koma cimeneci sicinakondweretsa Samueli, pamene iwo
anati, Tipatseni mfumu kuti itiweruze. Ndipo Samueli anapemphera
kwa Yehova. 7Ndipo Yehova ananena ndi Samueli, Umvere mau
onse anthuwo alikulankhula nawe; popeza sindiwe anakukana,
koma ndine anandikana, kuti ndisakhale mfumu yao. 8Monga
nchito zao zonse anazicita kuyambira tsiku lija ndinawaturutsa ku
Aigupto, kufikira lero lino kuti anandisiya Ine, natumikira milungu
yina, momwemo alikutero ndi iwenso. 9Cifukwa cace tsono umvere
mau ao koma uwacenjeze kolimba, ndi kuwadziwitsa makhalidwe
ace a mfumu imene idzawaweruza.
10Ndipo Samueli anauza anthu akumpempha iye mfumu mau onse
a Yehova, 11Nati, Awa ndi makhalidwe a mfumu imene idzaweruza
inu; idzatenga ana anu amuna, akhale akusunga magareta, ndi
akavale ace; ndipo adzathamanga ndi kutsogolera magareta
ace; 12idzawaika akhale otsogolera cikwi, ndi otsogolera makumi
asanu; ndipo idzaika ena kulima minda yace, ndi kutema dzinthu
zace, ndi kumpangira zipangizo za nkhondo, ndi zipangizo za
magareta. 13Ndipo idzatenga ana anu akazi apange zonunkhira,
naphikire, naumbe mikate. 14Ndipo idzalanda minda yanu, ndi
minda yamphesa yanu, ndi minda yaazitona, inde minda
yoposayo, nidzaipatsa anyamata ace. 15Ndipo idzatenga limodzi la
magawo khumi la mbeu zanu, ndi la minda yanu yamphesa,
nidzalipatsa akapitao ace, ndi anyamata ace. 16Ndipo idzatenga
akapolo anu, ndi adzakazi anu, ndi anyamata anu okongola
koposa, ndi aburu anu, nidzawagwiritsa nchito yace. 17Idzatenga
limodzi la magawo khumi la zoweta zanu; ndipo inu mudzakhala
akapoloace. 18Ndipotsiku lija mudzapfuula cifukwa ca mfumu yanu
munadzisankhira nokha; koma Yehova sadzayankha inu tsiku
lijalo. 19Koma anthu anakana kumvera mau a Samueli; nati, Iai,
koma tifuna kukhala nayo mfumu yathu; 20kuti ifenso tikafanane
nao anthu a mitundu yonse; kuti mfumu yathuyo ikatiweruzire, ndi
kuturuka kutitsogolera, ndi kuponya nafe nkhondo zathu. 21Ndipo

Samueli anamva mau onse a anthuwo, nawafotokozanso
m'makutu a Yehova. 22Ndipo Yehova anati kwa Samueli, Umvere
mau ao, nuwalongere mfumu, Ndipo Samueli anati kwa amuna a
Israyeli, Mupite, munthu yense ku mudziwace.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Sauli afuna aburu olowerera a atate wace

1Ndipo panali munthu Mbenlamlni, dzina lace ndiye Kisi, mwana
wa Abiyeli, mwana wa Zerori, mwana wa Bekorati, mwana wa
Afiya, mwana wa Mbenjamini, ndiye ngwazi. 2Iye anali ndi mwana
wamwamuna dzina lace Sauli, mnyamata wokongola; pakati pa
anthu onse a Israyeli panalibe wina wokongola ngati iye; anali
wamtali, anthu onse ena anamlekeza m'cifuwa. 3Ndipo aburu a
Kisi, atate wa Sauli, analowerera. Ndipo Kisi anati kwa Sauli mwana
wace, Utenge mnyamata mmodzi, nunyamuke, kukafuna
aburuwo. 4Ndipo anapyola dziko lamapiri la Efraimu, napyola dziko
la Salisa, koma sanawapeza; pamenepo anapyolanso dziko la
Salimu; koma panalibe pamenepo, napyola dziko la Abenjamini,
osawapeza. 5Pamene anafika ku dziko la Zufi, Sauli anamuuza
mnyamata amene anali naye, kuti, Tiye tibwerere; kuti atate
wanga angaleke kusamalira aburuwo, ndi kutenga nkhawa cifukwa
ca ife. 6Koma ananena naye, Onatu, m'mudzi muno muli munthu
wa Mulungu, ndiye munthu anthu amcitira ulemu; zonse azinena
zicitika ndithu; tiyeni tipite komweko, kapena adzakhoza
kutidziwitsa zimene tirikuyendera. 7Ndipo Sauli ananena ndi
mnyamata wace, Koma taona, tikapitako nmtengere ciani
munthuyo? popeza mkate udatha m'zotengera zathu, ndiponso
tiribe mphatso yakumtengera munthu wa Mulungu, tiri naco
ciani? 8Ndipo mnyamatayo anayankhanso kwa Sauli nati, Onani
m'dzanja langa muli limodzi la magawo anai a sekeli wa siliva;
ndidzampatsa munthu wa Mulungu limeneli kuti atiuze njira
yathu. 9Kale m'Israyeli, munthu akati afunse kwa Mulungu,
adafotero kuti, Tiyeni tipite kwa mlauliyo; popeza iye wochedwa
mneneri makono ano, anachedwa mlauli kale. 10Pamenepo Sauli
anati kwa mnyamata wace, Wanena bwino; tiye tipite. Comweco
iwowa anapita kumudzi kumene kunali munthu wa
Mulunguyo. 11Pakukwera kumudziko anapeza anthu akazi
alikuturuka kuti akatunge madzi, nanena nao, Mlauliyo alipo
kodi? 12Ndipo anawayankha nati, Alipo; onani ali m'tsogolo mwanu;
fulumirani pakuti wabwera lero kumudzi kuno; popeza lero anthu
akuti aphere nsembe pamsanje; 13mutafika m'mudzi, pomwepo
mudzampeza, asanakwere kumsanje kukadya; pakuti anthu
sadzadya, koma iye atafika ndipo; pakuti iye amadalitsa
nsembeyo; ndipo atatero oitanidwawo amadya. Cifukwa cace
kwerani; popeza nthawi yino mudzampeza. 14Ndipo iwowa
anakwera kumudzi; ndipo m'mene analowa m'mudzimo, onani,
Samueli anaturukira pali Iwo, kuti akakwere kumsanje.

Sauli akomana ndi Samueli

15Ndipo Yehova anaululiratu m'khutu la Samueli dzulo lace la tsiku
limene Sauli anabwera, kuti, 16Mawa, monga dzuwa lino,
ndidzakutumizira munthu wocokera ku dziko la Benjamini,
udzamdzoza iye akhale mtsogoleri wa anthu anga Israyeli, kuti
akawapulumutse anthu anga m'manja a Afilisti; pakuti Ine
ndinapenya pa anthu anga, popeza kulira kwao kunandifika
Ine. 17Ndipo pamene Samueli anaona Sauli, Yehova anati kwa iye,
Ona munthu amene ndinakuuza za iye! ameneyu adzaweruza
anthu anga. 18Pomwepo Sauli anayandikira kwa Samueli pakati pa
cipata, nati, Mundidziwitse nyumba ya mlauliyo iri kuti. 19Ndipo
Samueli anayankha Sauli nati, Inendinemlauliyo. Kwera, batsogola
kumsanje, pakuti mudzadya ndi ine lero; ndipo m'mawa
ndidzakulola upite, ndi kukudziwitsa zonse ziri mumtima
mwako. 20Za aburu ako atatayika adapita masiku atatu,
usalingalirenso iwowa; pakuti anapezedwa. Ndipo cifuniro conse ca
Israyeli ciri kwa yani? Si kwa iwe ndi banja lonse la atate
wako? 21Ndipo Sauli anayankha nati, Sindiri Mbenjamini kodi, wa
pfuko laling'ono mwa Israyeli? Ndiponso banja lathu nlocepa pakati
pa mabanja onse a pfuko la Benjamini? Potero mulankhula bwanji
mau otere ndi ine? 22Ndipo Samueli anatenga Sauli ndi mnyamata
wace, napita nao ku cipinda ca alendo, nawakhalitsa pa malo a
ulemu pakati pa oitanidwa onse; ndiwo anthu monga makumi
atatu. 23Ndipo Samueli ananena ndi wophika, Tenga nyama
ndinakupatsa, ndi kuti, Ibakhala ndi iwe. 24Ndipo wophikayo
ananyamula mwendo ndi mnofu wace, nauika pamaso pa Sauli.
Ndipo Samueli anati, Onani cimene tinakuikirani muciike pamaso
panu, nudye; pakuti ici anakuikirani kufikira nthawi yonenedwa,
popeza ndinati, Ndinaitana anthuwoo Comweco Sauli anadya ndi
Samueli tsiku lija. 25Ndipo pamene anatsika kumsanje kulowanso
kumudzi, iye anakamba ndi Sauli pamwamba pa nyumba
yace. 26Ndipo anauka mamawa; ndipo kutaca, Samueli anaitana
Sauli ali pamwamba pa nyumba, nati, Ukani kuti ndikuloleni
mumuke. Ndipo Sauli anauka, naturuka onse awiri, iye ndi Samueli,
kunka kunja. 27Ndipo pamene analikutsika polekeza mudzi,
Samueli ananena ndi Sauli, Uzani mnyamatayo abatsogola; napita
iyeyo. Koma inu muime pano, kuti ndikumvetseni mau a Mulungu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Samueli; adzoza Sauli akhale mfumu ya Israyeli

1Pamenepo Samueli anatenga nsupa ya mafuta, nawatsanulira
pamutu pace, nampsompsona iye, nati, Sanakudzozani ndi
Mulungu kodi, mukhale mfumu ya pa colowa cace? 2M'mene
talekana lero, mudzakomana ndi anthu awiri pa manda a Rakele,
pa malire a Benjamini ku Zeliza; iwo ndiwo adzanena nanu, Aburu
aja munakafuna, anapezedwa; ndipo onani, atate wanu analeka
kulingalira aburuwo, koma alikulingalira za inu, ndi kuti, Ndidzacita
ciani, cifukwa ca mwana wanga? 3Mukapitirira pamenepo tsono ndi
kufika ku mtengo wathundu wa ku Tabori, kumeneko adzakomana
nanu anthu atatu akukwera kwa Mulungu ku Beteli, wina
wonyamula ana a mbuzi atatu, wina mikate itatu, wina thumba la
vinyo. 4Iwowa adzakulankhulani, ndi kukupatsani mikate iwiri;
imeneyi mudzailandira m'manja mwao. 5Ndipo m'tsogolo mwace
mudzafika ku phiri la Mulungu, kumene kuli kaboma ka Afilisti;
ndipo kudzali kuti pakufika inu kumudziko mudzakomana ndi gulu
la aneneri, alikutsika kumsanje ndi cisakasa, ndi lingaka, ndi toliro,
ndi zeze, pamaso pao; iwo adzanenera; 6ndipo Mzimu wa Yehova
udzagwera inu kolimba, nanunso mudzanenera pamodzi nao,
nimudzasandulika munthu wina. 7Ndipo zitakufikirani zizindikilo izi
mudzacita monga mudzaona pocita, pakuti Mulungu ali
nanu. 8Ndipo mudzatsika patsogolo pa ine kunka ku Giligala; ndipo,
taonani, ndidzatsikira kwa inu kukapereka zopsereza, ndi kuphera
nsembe zamtendere. Mutsotsepo masiku asanu ndi awiri kufikira
ndikatsikira kwa inu ndi kukudziwitsani cimene mudzacita. 9Ndipo
kunali, pamene iye anapotoloka kuti alekane ndi Samueli, Mulungu
anampatsa mtima wina watsopano; ndipo zizindikilo zija zonse
zinacitika tsiku lija.

Sauli pakati pa aneneri

10Ndipo pamene anafika kucitunda kuja, onani, gulu la aneneri
linakomana naye; ndi Mzimu wa Mulungu unamgwera
mwamphamvu, iye nanenera pakati pao, 11Ndipo kunali, kuti onse
amene anamdziwiratu kale, pakuona ici cakuti, onani, iye
ananenera pamodzi ndi aneneri, anati wina ndi mnzace, Ici nciani
cinamgwera mwana wa Kisi? Kodi Saulinso ali mwa
aneneri? 12Ndipo munthu wina wa komweko anayankha nati, Ndipo
atate wao ndiye yani? Cifukwa cace mauwa anakhala ngati
mwambi, Kodi Saulinso ali mwa aneneri? 13Ndipo pamene adatha
kunenera anafika kumsanjeko.
14Ndipo mbale wa atate wace wa Sauli ananena kwa iye ndi
mnyamata wace, Munanka kuti? Ndipo iye anati, Kukafuna
aburuwo; ndipo pakuona kuti sitinawapeza, tinadza kwa
Samueli. 15Ndipo mbale wa atate wa Sauli anati, Undiuze cimene

Samueli analankhula nawe. 16Ndipo Sauli anati kwa mbale wa
atate wace, Anatiuza momveka kuti aburuwo anapezedwa kale.
Koma sanamdziwitsa mau aja Samueli ananena zaufumuwo.

Anthu abvomereza Sauli akhale mfumu yao

17Ndipo Samueli anaitana anthu onse asonkhane kwa Yehova ku
Mizipa; 18nanena ndi ana a Israyeli, Atero Yehova, Mulungu wa
Israyeli kuti, Ine ndinaturutsa Israyeli m'Aigupto, ndipo
ndinakupulumutsani m'manja a Aaigupto, ndi m'manja a maufumu
onse anakusautsani; 19koma lero inu mwakana Mulungu wanu
amene anakupulumutsani yekha m'matsoka anu onse, ndi
m'masautso anu; ndipo munanena naye, Koma mutipatse mfumu.
Cifukwa cace tsono mudzionetse pamaso pa Mulungu mafuko
mafuko, ndi magulu magulu. 20Comweco Samueli anayandikizitsa
mafuko onse a Israyeli, ndipo pfuko la Benjamini
linasankhidwa. 21Nayandikizitsa pfuko la Benjamini, banja ndi
banja, ndipo banja la Amatiri linasankhidwa; nasankhidwa Sauli
mwana wa Kisi. Koma pamene anamfuna, anapeza
palibe. 22Cifukwa cace anaonjeza kufunsa Yehova, Watsala wina
kodi woyenera kubwera kuno? Ndipo Yehova anati, Onani,
alikubisala pakati pa akatundu. 23Ndipo anathamanga, namtenga
komweko; ndipo iye pamene anaima pakati pa anthuwo, anali
wamtali koposa anthu onse anamlekeza m'cifuwa. 24Ndipo Samueli
ananena ndi anthu onse, Mumuona kodi iye amene Yehova
anamsankha, kuti palibe wina wakufanana naye pakati pa anthu
onse? Ndipo anthu onse anapfuula, kuti, Akhale ndi moyo
mfumuyo.

25Pamenepo Samueli anafotokozera anthu macitidwe a ufumu,
nawalembera m'buku, nalisunga pamaso pa Yehova. Ndipo
Samueli anauza anthu onse amuke, yense ku nyumba yace, 26Ndi
Sauli yemwe anamuka ku nyumba yace ku Gibeya; ndipo
am'khamu anatsagana naye iwo amene Mulungu adakhudza
mitima yao. 27Koma oipa ena anati, Uyu adzatipulumutsa bwanji?
Ndipo anampeputsa, osakampatsa mtulo. Koma iye anakhala cete.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Sauli alanditsa Yabezi Gileadi m'manja mwa Aamoni

1Pamenepo Nahasi M-amoni anakwera, namanga Yabezi Gileadi
zithando; ndipo anthu onse a ku Yabezi anati kwa Nahasi,
Mupangane cipangano ndi ife, ndipo tidzakutumikirani inu. 2Ndipo
Nahasi Mamoni ananena nao, Ndidzapangana nanu, ngati mulola
kuti maso a ku dzanja lamanja anu onse akolowoledwe; potero
ndidzanyazitsa Aisrayeli onse. 3Ndipo akuru a ku Yabezi ananena
naye, Mutipatse masiku asanu ndi awiri, kuti titumize mithenga
m'malire onse a Israyeli; ndipo pakapanda kuoneka wotipulumutsa
ife, tidzaturukira kwa inu. 4Tsono mithengayo inafika ku Gibeya
kwa Sauli, nalankhula mau amenewa m'makutu a anthu; ndipo
anthu onse anakweza mau, nalira misozi. 5Ndipo, onani, Sauli
anacokera kumunda alikutsata ng'ombe; nati Sauli, Coliritsa anthu
misozi nciani? Ndipo anamuuza mau a anthu a ku Yabezi. 6Ndipo
mzimu wa Mulungu unamgwera Sauli mwamphamvu, pamene
anamva mau awa, ndi mkwiyo wace unayaka kwambiri. 7Natenga
ng'ombe ziwiri nazidula nthuli nthuli, nazitumiza m'malire monse
mwa Israyeli, ndi dzanja la mithenga, nati, Amene sakudza
pambuyo pa Sauli ndi pa Samueli, adzatero nazo ng'ombe zace.
Ndipo kuopsa kwa Yehova kunawagwera anthu, naturuka ngati
munthu mmodzi. 8Ndipo anawawerenga ku Bezeki; ndipo ana a
Israyeli anali zikwi mazana atatu, ndi anthu a Yuda ndiwo zikwi
makumi atatu. 9Ndipo anati kwa mithenga inadzayi, Muzitero kwa
anthu a ku Yabezi Gileadi, Mawa litatentha dzuwa, mudzaona
cipulumutso. Ndipo mithenga inadza niuza a ku Yabezi;
nakondwara iwowa. 10Cifukwa cace anthu a ku Yabezi anati, Mawa
tidzaturukira kwa inu, ndipo mudzaticitira cokomera inu. 11Ndipo
m'mawa mwace Sauli anagawa anthu magulu atatu; ndipo iwowa
anafika pakati pa zithandozo m'ulonda wa mamawa, nakantha
Aamoni kufikira kutentha kwa dzuwa. Ndipo otsalawo anabalalika,
osatsala pamodzi ngakhale awiri. 12Ndipo anthu anati kwa
Samueli, Ndani iye amene anati, Kodi Sauli adzatiweruza ife?
tengani anthuwo kuti tiwaphe. 13Koma Sauli anati, Sadzaphedwa
lero munthu; pakuti lero Yehova anacita cipulumutso m'Israyeli.
14Ndipo Samueli ananena kwa anthuwo, Tiyeni tipite ku Giligala,
kukonzanso ufumu kumeneko. 15Ndipo anthu onse anapita ku
Giligala; ndi kumeneko analonga Sauli mfumu pamaso pa Yehova
m'Giligala; ndi pamenepo anaphera nsembe zoyamika pamaso pa
Yehova; ndi pomwepo Sauli ndi anthu onse a Israyeli anakondwera
kwakukuru.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Samueli adzinenera kwa anthu

1Ndipo Samueli anauza Aisrayeli onse, kuti, Onani dani ndinamvera
mau anu mwa zonse munalankhula ndi ine, ndipo
ndinakulongerani mfumu. 2Ndipo tsopano, siyi mfumu idzayendabe
pamaso panu; ndipo ine ndine wokalamba waimvi; ndipo, onani,
ana anga amuna ali nanu, ndipo ine ndinayendabe pamaso panu
kuyambira ubwana wanga kufikira lero. 3Ndikalipo ine; citani
umboni wonditsutsa pamaso pa Yehova, ndi pamaso pa
wodzozedwa wace; ndinalanda ng'ombe ya yani? kapena
ndinalanda buru wa yani? ndinanyenga yani? ndinasautsa yani?
ndinalandira m'manja mwa yani cokometsera mlandu kutseka
naco maso anga? ngati ndinatero ndidzacibwezera kwa inu. 4Ndipo
iwo anati, Simunatinyenga, kapena kutisautsa, kapena kulandira
kanthu m'manja mwa wina ali yense. 5Ndipo iye ananena nao,
Yehova ali mboni yanu, ndi wodzozedwa wace ali mboni lero kuti
simunapeza kanthu m'dzanja langa, Nati iwo, iye ali mboni. 6Ndipo
Samueli ananena ndi anthuwo, Yehova ndiye amene anaika Mose
ndi Aroni, naturutsanso makolo anu m'dziko la Aigupto, 7Cifukwa
cace tsono, imani pano, kuti ndiweruzane nanu pamaso pa Yehova
za nchito zonse zolungama za Yehova, anakucitirani inu ndi makolo
anu. 8Pamene Yakobo anafika ku Aigupto, ndi makolo anu
anapemphera kwa Yehova, Yehova anatumiza Mose ndi Aroni,
amene anaturutsa makolo anu m'Aigupto, nawakhalitsa pamalo
pano, 9Koma iwowa anaiwala Yehova Mulungu wao, iye
nawapereka m'dzanja la Sisera kazembe wa gulu la Hazori, ndi
m'dzanja la Afilisti, ndi m'dzanja la mfumu ya Moabu, iwo
naponyana nao. 10Ndipo anapemphera kwa Yehova, kuti,
Tinacimwa, popeza tinasiya Yehova, ndi kutumikira Abaala ndi
Asitaroti, koma mutipulumutse tsopano m'manja a adani anthu,
ndipo tidzakutumikirani Inu. 11Ndipo Yehova anatumiza Yerubaala,
ndi Bedani, ndi Yefita, ndi Samueli, napulumutsa inu m'manja mwa
adani anu pozungulira ponse, ndipo munakhala
mosatekeseka. 12Ndipo pamene munaona kuti Nahasi mfumu ya
ana a Amoni inadza kuponyana nanu, munanena ndi ine, Koma
mfumu itiweruze; ngakhale mfumu yanu ndiye Yehova Mulungu
wanu. 13Cifukwa cace siyi mfumu imene munaisankha, imene
munandipempha; ndipo taonani, Yehova anakuikirani
mfumu. 14Mukaopa Yehova ndi kumtumikira ndi kumvera mau ace,
ndi kusakana lamulo lace la Yehova, ndipo inu ndi mfumu imene
iweruza inu mukadzatsata Yehova Mulungu wanu, cabwino. 15Koma
mukapanda kumvera mau a Yehova, ndi kupikisana ndi lamulo la
Yehova, dzanja la Yehova lidzatsutsana nanu, monga linatsutsana
ndi makolo anu. 16Cifukwa cace tsono, imani pano, muone cinthu

ici cacikuru Yehova adzacicita pamaso panu. 17Si nyengo
yakumweta tirigu lero kodi? Ndidzaitana kwa Yehova, kuti atomize
bingu ndi mvula; ndipo mudzazindikira ndi kuona kuti coipa canu
munacicita pamaso pa Yehova ndi kudzipemphera mfumu,
ncacikuru. 18Momwemo Samueli anaitana kwa Yehova; ndipo
Yehova anatumiza bingu ndi mvula tsiku lomwelo; ndipo anthu
onse anaopa kwambiri Yehova ndi Samueli. 19Ndipo anthu onse
ananena ndi Samueli, Mupempherere akapolo anu kwa Yehova
Mulungu wanu, kuti tingafe; popeza pamwamba pa zoipa zathu
zonse tinaonjeza coipa ici, cakuti tinadzipemphera mfumu. 20Ndipo
Samueli ananena kwa anthuwo, Musaope; munacitadi coipa ici
conse, koma musaleka kutsata Yehova, koma mutumikire Yehova
ndi mtima wanu wonse; 21musapambukire inu kutsata zinthu
zacabe, zosapindulitsa, zosapulumutsa, popeza ziri zopanda
pace. 22Pakuti Yehova sadzasiya anthu ace cifukwa ca dzina lace
lalikuru; pakuti kudamkomera Yehova kukuyesani inu anthu a iye
yekha. 23Ndipo inenso, kukhale kutali ndi ine, kucimwira Yehova
ndi kuleka kukupempherera ni; koma ndidzakulangizani njira
yabwino ndi yolungama. 24Koma mumuope Yehova, ndi
kumtumikira koona, ndi mtima wanu wonse; lingalirani zinthu
zazikuruzo iye anakucitirani. 25Koma mukaumirirabe kucita coipa,
mudzaonongeka, inu ndi mfumu yanu yomwe.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Nkhondo pakati pa Israyeli ndi Afilisti

1Sauli anali ndi zaka makumi atatu pamene anayamba ufumu
wace; nakhala mfumu ya Israyeli zaka ziwiri. 2Pamenepo Sauli
anadzisankhira anthu zikwi zitatu a Israyeli; zikwi ziwiri za iwowa
zinali ndi Sauli ku Mikimasi, ndi ku phiri la ku Beteli; ndi cikwi
cimodzi anali ndi Jonatani ku Gibeya wa ku Benjamini; ndipo
anawauza anthu ena onse amuke ku mahema ao. 3Ndipo Jonatani
anathyola kaboma ka Afilisti lokhala ku Geba, ndipo Afilisti anamva
za ici. Ndipo Sauli analiza lipenga m'dziko monse, nati, Amve
Ahebri. 4Ndipo Aisrayeli onse anamva kunena kuti Sauli anathyola
kaboma ka Afilisti, ndi kuti Afilisti anyansidwa ndi Aisrayeli. Ndipo
anthuwo anasonkhana kwa Sauli ku Giligala.
5Ndipo Afilisti anasonkhana kuti akamenyane ndi Aisrayeli, anali
nao magareta zikwi makumi atatu, ndi apakavalo zikwi zisanu ndi
cimodzi, ndi anthu akucuruka monga mcenga wa pa dooko la
nyanja. Iwowa anakwera namanga zithando ku Mikimasi
kum'mawa kwa Betaveni. 6Pamene anthu a Israyeli anazindikira
kuti ali m'kupsinjika, pakuti anthuwo anasauka mtima, anthuwo
anabisala m'mapanga, ndi m'nkhalango, ndi m'matanthwe, ndi
m'malinga, ndi m'maenje. 7Ndipo Ahebri ena anaoloka Yordano
nafika ku dziko la Gadi ndi Gileadi; koma Sauli akali ku Giligala,
ndipo anthu onse anamtsata ndi kunthunthumira.

Samueli adzudzula Sauli pa kupereka iye nsembe

8Ndipo iye anatsotsa masiku asanu ndi awiri, monga nthawi
anampanga Samueli; koma Samueli sanafika ku Giligala, ndipo
anthu anabalalika namsiya Sauli. 9Pamenepo Sauli anati,
Andipatsire kuno nsembe yopsereza, ndi nsembe zoyamika. Ndipo
iye anapereka nsembe yopserezayo. 10Ndipo kunali kuti pakutsiriza
iye kupereka nsembe yopserezayo, pomwepo, onani, Samueli
anafika. Ndipo Sauli anamcingamira kukamlankhula iye. 11Ndipo
Samueli anati, Mwacitanji? Nati Sauli, Cifukwa ndinaona kuti
anthuwo alinkubalalika kundisiya ine, ndi kuti inu simunafika
masiku aja tinapangana, ndi kuti Afilisti anasonkhana ku
Mikimasi; 12cifukwa cace ndinati, Afilisti adzatitsikira pane pa
Giligala, ndisanapembedze Yehova; potero ndinadzifulumiza, ndi
kupereka nsembe yopsereza. 13Ndipo Samueli ananena ndi Sauli,
Munacita kopusa; simunasunga lamulo la Yehova Mulungu wanu,
limene iye anakulamulirani; mwenzi Yehova atakhazikitsa nthawi
yino ufumu wanu, ukhale pa Israyeli nthawi yosatha. 14Koma
tsopano ufumu wanu sudzakhala cikhalire; Yehova wadzifunira
munthu wa pamtima pace; ndipo Yehova wamuika iye akhale
mtsogoleri wa anthu ace, cifukwa inu simunasunga cimene Yehova
anakulamulirani.

15Ndipo Samueli anauka nacoka ku Giligala kunka ku Gibeya wa ku
Benjamini. Ndipo Sauli anawerenga anthu amene anali naye,
monga mazana asanu ndi limodzi. 16Ndipo Sauli, ndi Jonatani
mwana wace, ndi anthu akukhala nao anakhala ku Geba wa ku
Benjamini; koma Afilistiwo anali nazo zithando zao ku
Mikimasi. 17Ndipo owawanya anaturuka ku zithando za Afilisti
magulu atatu; gulu limodzi linalowa njira yonka ku Ofra, ku dera la
Sauli; 18gulu lina linalowa njira yonka ku Betihoroni; ndi gulu
linanso linalowa ku njira ya kumalire, akuyang'ana ku cigwa ca
Zeboimu kucipululuko.
19Ndipo m'dziko lonse la Israyeli simunapezeka wosula; popeza
Afilisti adati, Kuti Aisrayeli angadzisulire malupanga kapena
mikondo; 20koma Aisrayeli onse adafotsikira kwa Afilisti, kuti
awasaniire munthu yense cikhasu cace, colimira cace, nkhwangwa
yace, ndi khasu lace; 21koma analf nao matupa kukonza makasu,
ndi zikhasu ndi makasu a mana ndi nkhwangwazo; ndi kusongola
zothwikira. 22Comweco kunali kuti tsiku lankhondolo sunapezeka
mkondo kapena lupanga m'manja a anthu onse anali ndi Sauli ndi
Jonatani; koma Sauli yekha ndi Jonatani mwana wace anali
nazo. 23Ndipo a ku kaboma ka Afilisti anaturuka kunka ku mpata
wa ku Mikimasi.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Jonatani agonjetsa Afilisti

1Ndipo kunali tsiku lina kuti Jonatani mwana wa Sauli ananena ndi
mnyamata wonyamula zida zace, Tiye tipite kunka ku kaboma ka
Afilisti, tsidya lija. Koma sanauza atate wace. 2Ndipo Sauli
analikukhala m'matsekerezo a Gibeya patsinde pa mtengo
wankhangaza uli ku Migroni; ndipo panali naye anthu monga
mazana asanu ndi limodzi; 3ndi Ahiya mwana wa Ahitubi mbale
wace wa Ikabodi, mwana wa Pinehasi, mwana wa Eli, wansembe
wa Yehova wa ku Silo, wobvala efodi. Ndipo anthuwo sanadziwa
kuti Jonatani wacoka. 4Ndipo pakati pa mipata imene Jonatani
anafuna kupitapo kunka ku kaboma ka Afilisti, panali phiri
lathanthwe pa mbali yina, ndi phiri lathanthwe pa mbali inzace;
ndipo dzina la linalo ndilo Bozezi, ndi la linzace ndilo Sene. 5Phiri
lija linaimirira kuyang'ana kumpoto pandunji pa Mikimasi, ndi
linzace kumwera pandunji pa Geba. 6Ndipo Jonatani ananena ndi
mnyamata wonyamula zida zace, Tiye tipite ku kaboma ka
osadulidwa awa; kapena Yehova adzatigwirira nchito; pakuti palibe
comletsa Yehova kupulumutsa angakhale ndi ambiri kapena ndi
owerengeka. 7Ndipo wonyamula zida zace ananena naye, Citani
zonse ziri mumtima mwanu; palukani, onani ndiri pamodzi ndi inu
monga mwa mtima wanu. 8Ndipo Jonatani anati, Taona, ife
tidzapita kunka kwa anthuwo, ndipo tidzadziu lula kwa
iwo. 9Akatero ndi ife kuti, Baimani kufikira titsikira kwa inu; tsono
tidzaima m'malo mwathu, osakwera kwa iwo. 10Koma akatero kuti,
Kwerani kuno kwa ife, tsono tidzakwera; pakuti Yehova
wawapereka m'manja mwathu; ndipo ici cidzatikhalira
cizindikilo. 11Ndipo onse awiri anadziulula kwa a ku kaboma ka
Afilistiwo; ndipo Afilistiwo anati, Onani, Ahebri alikuturuka
m'mauna m'mene anabisala. 12Ndipo a ku kabomawo anayankha
Jonatani ndi wonyamula zida zace, nati, Kwerani kuno kwa ife,
tikuonetseni kanthu. Ndipo Jonatani anauza wonyamula zida zace,
Kwera unditsate m'mbuyo, pakuti Yehova wawapereka m'dzanja la
Israyeli. 13Ndipo Jonatani anakwera cokwawa, ndi wonyamula zida
zace anamtsata; ndi Afilisti anagwa pamaso pa Jonatani, ndi
wonyamula zida zace anawapha pambuyo pace. 14Kuwapha
koyambako, Jonatani ndi wonyamula zida zace, anapha monga
anthu makumi awiri, monga ndime ya munda yolima ng'ombe
ziwiri tsiku limodzi. 15Ndipo kunali kunthunthumira kuzithando,
kuthengoko, ndi pakati pa anthu onse; a ku kaboma ndi owawanya
omwe ananthunthumira; ndi dziko linagwedezeka; comweco kunali
kunthunthumira kwakukuru koposa, 16Ndipo ozonda a Sauli ku
Gibeya wa ku Benjamini anayang'ana; ndipo, onani, khamu la
anthu linamwazikana, kulowa kwina ndi kwina.

Sauli alumbirira anthu

17Pamenepo Sauli ananena ndi anthu amene anali naye, Awerenge
tsopano, kuti tizindikire anaticokera ndani. Ndipo pamene
anawerenga, onani Jonatani ndi wonyamula zida zace
panalibe. 18Ndipo Sauli ananena ndi Ahiya, Bwera nalo likasa la
Mulungu kuno. Pakuti likasa la Mulungu linali kumeneko masiku aja
ndi ana a Israyeli. 19Ndipo kunali m'mene Sauli anali cilankhulire
ndi wansembeyo, phokoso la m'cigono ca Afilisti linacitikabe,
nilikula; ndipo Sauli ananena ndi wansembeyo, Bweza dzanja
lako. 20Ndipo Sauli ndi anthu onse amene anali naye anaunjikana
pamodzi, naturukira kunkhondoko; ndipo taonani, munthu yense
anakantha mnzace ndi lupanga, ndipo panali kusokonezeka
kwakukuru. 21Ndiponso Ahebri akukhala nao Afilisti kale, amene
anaturuka m'dziko lozungulira kukaiowa nao kuzithando; iwonso
anatembenukira kuti akakhale ndi Aisrayeli amene anali ndi Sauli
ndi Jonatani. 22Anateronso Aisrayeli onse akubisala m'phiri la
Efraimu, pakumva kuti Afilisti anathawa, iwo anawapitikitsa
kolimba kunkhondoko. 23Comweco Yehova anapulumutsa Israyeli
tsiku lija; ndipo nkhondo inapitirira pa Betaveni. 24Ndipo Aisrayeli
anasauka tsiku lija; pakuti Sauli anawalumbirira, kuti,
Atembereredwe iye wakudya kanthu kufikira madzulo,
ndikabwezere cilango adani anga. Motero anthu onse anakhala
opanda kudya. 25Ndipo anthu onsewo analowa munkhalango,
panali uci pansi. 26Ndipo pakufika anthuwo m'nkhalangomo, onani,
madzi a uci anacuruka; koma panalibe munthu mmodzi anaika
dzanja lace pakamwa, pakuti anthuwo anaopa
tembererolo. 27Koma Jonatani sanamva m'mene atate wace
analumbirira anthu; cifukwa cace iye ana tam balitsa ndodo ya
m'dzanja lace, naitosa m'cisa ca uci, naika dzanja lace pakamwa
pace; ndipo m'maso mwace munayera. 28Ndipo wina wa anthuwo
anayankha, nati, Atate wanu analangiza anthu kolimba ndi
lumbiro, ndi kuti, Wotembereredwa iye wakudya lero cakudya.
Ndipo anthuwo analema. 29Ndipo Jonatani anati, Atate wanga
wabvuta dziko; onani m'maso mwanga mwayera, cifukwa
ndinalawako pang'ono uciwu. 30Koposa kotani nanga, ngati anthu
akadadya nakhuta zowawanya anazipeza za adani ao? popeza
tsopano palibe kuwapha kwakukuru kwa Afilisti. 31Ndipo anakantha
Afilisti tsiku lija kuyambira ku Mikimasi kufikira ku Ajaloni, ndipo
anthu anafoka kwambiri. 32Ndipo anthuwo anathamangira
zowawanyazo, natenga nkhosa, ndi ng'ombe, ndi ana a ng'ombe,
naziphera pansi; anthu nazidya ziri ndi mwazi wao. 33Pamenepo
anauza Sauli, kuti, Onani anthu alikucimwira Yehova, umo akudya
zamwazi. Ndipo iye anati, Munacita konyenga; kunkhunizani mwala
waukuru kwa ine lero. 34Ndipo Sauli anati, Balalikani pakati pa

anthu, nimuwauze kuti abwere kwa ine kuno munthu yense ndi ng'ombe yace, ndi munthu yense ndi nkhosa yace, aziphe pano, ndi kuzidya, osacimwira Yehova ndi kudya zamwazi. Nabwera anthu onse, yense ndi ng'ombe yace, usiku uja naziphera pomwepo. 35Ndipo Sauli anamangira Yehova guwa la nsembe; limenelo ndilo guwa loyamba iye anamangira Yehova.

Jonatani atsutsidwa ale

36Ndipo Sauli anati, Tiyeni titsikire usiku kwa Afilistiwo, ndi kuwawawanya kufikira kutayera, tisasiye munthu mmodzi wa iwowa. Ndipo iwo anati, Citani ciri conse cikukomerani. Pamenepo wansembeyo anati, Tisendere kwa Yehova kuno. 37Ndipo Sauli anafunsira uphungu kwa Mulungu, Nditsikire kodi kwa Afilisti? Mudzawapereka m'dzanja la Israyeli kodi? Koma iye sanamyankha tsiku lomweli. 38Ndipo Sauli anati, Musendere kuno, inu nonse akuru a anthu; kuti muzindikire ndi kuona m'mene muli coipa ici lero. 39Pakuti, pali Yehova wakupulumutsa Israyeli, cingakhale ciri m'mwana wanga Jonatani, koma adzafa ndithu. Koma pakati pa anthu onse panalibe mmodzi wakumyankha iye. 40Ndipo iye ananena ndi Aisrayeli onse, Inu mukhale mbali yina, ndipo me ndi Jonatani mwana wanga tidzakhala mbali yinanso. Ndipo anthuwo ananena ndi Sauli, Citani cimene cikukomerani. 41Cifukwa cace Sauli ananena ndi Yehova, Mulungu wa Israyeli, muonetse coonadi. Ndipo maere anagwera Sauli ndi Jonatani; koma anthuwo anapulumuka. 42Ndipo Sauli anati, Mucite maere pakati pa ine ndi Jonatani mwana wanga. Ndipo anagwera Jonatani. 43Pamenepo Sauli ananena ndi Jonatani, Undiuze cimene unacita. Ndipo Jonatani anamuuza, nati, Zoonadi ndinangolawako uci pang'ono ndi nsonga ya ndodo inali m'dzanja langa: ndipo onani ndiyenera kufa. 44Pamenepo Sauli anati, Mulungu andilange, naoniezereko, pakuti udzafa ndithu, Jonatani.

Anthu alanditsa Jonatani

45Ndipo anthuwo ananena ndi Sauli, Kodi Jonatani adzafa, amene anacititsa cipulumutso cacikuru ici m'Israyeli? Musatero. Pali Yehova, palibe tsitsi limodzi la pa mutu wace lidzagwa pansi, pakuti iye anagwirizana ndi Mulungu lero. Comweco anthuwo anapulumutsa Jonatani kuti angafe. Ndipo Sauli analeka kuwapitikitsa Afilistiwo; 46ndi Afilistiwo anamuka ku malo a iwo okha.

47Ndipo pamene Sauli atakhazikitsa ufumu wa pa Israyeli, iye anaponyana ndi adani ace onse pozungulira ponse, ndi Moabu, ndi ana a Amoni, ndi Edomu ndi mafumu a Zoba, ndi Afilisti; ndipo pali ponse anapotolokerapo, anawalanga. 48Ndipo iye anakula mphamvu, nakantha Aamaleki, napulumutsa Aisrayeli m'manja a akuwawawanya.

49Ndipo ana a Sauli ndiwo Jonatani, ndi Isivi, ndi Malikisuwa; ndi
maina a ana akazi ace awm ndi awa: dzina la woyamba ndiye
Merabu, ndi dzina la mng'ono wace ndiye Mikala; 50ndi dzina la
mkazi wa Sauli ndi Ahinamu mwana wa Ahimazi; ndi dzina la
kazembe wa khamu lankhondo lace ndiye Abineri mwana wa Neri,
mbale wace wa atate wa Sauli. 51Ndipo atate wa Sauli ndiye Kisi;
ndipo Neri atate wa Abineri ndiye mwana wa Abiyeli.
52Ndipo panali nkhondo yowawa ndi Afilisti masiku onse a Sauli;
ndipo Sauli pakuona munthu wamphamvu, kapena ngwazi,
anamtenga akhale naye.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Sauli alamulidwa aononge Amaleki

1Ndipo Samueli ananena ndi Sauli, Yehova ananditumiza ine
kukudzozani mukhale mfumu ya anthu ace Aisrayeli; cifukwa cace
tsono mumvere kunena kwa mau a Yehova. 2Atero Yehova wa
makamu, Ndinaonerera cimene Amaleki anacitira Israyeli, umo
anamlalira panjira, m'mene iye anakwera kuturuka
m'Aigupto. 3Muka tsopano, nukanthe Amaleki, nuononge konse
konse zonse ali nazo, usawalekerere, koma uwaphe mwamuna ndi
mkazi, mwana ndi woyamwa, ng'ombe ndi nkhosa, ngamila ndi
buru.
4Ndipo Sauli anamemeza anthu, nawawerenga ku Telayimu,
akuyenda pansi zikwi mazana awiri, ndi a kwa Yuda anthu zikwi
khumi. 5Ndipo Sauli anafika ku mudzi wa Amaleki, nalalira
kucigwa. 6Ndipo Sauli anauza Akeni kuti, Mukani, cokani mutsike
kuturuka pakati pa Aamaleki, kuti ndingakuononge pamodzi ndi
iwo; pakuti inu munacitira ana a Israyeli onse zabwino, pakufuma
iwo ku Aigupto. Comwece Akeni anacoka pakati pa
Aamaleki. 7Ndipo Sauli anakantha Aamaleki, kuyambira pa Havila,
dera la ku Suri; ciri pandunji pa Aigupto. 8Namtenga wamoyo
Agagi, mfumu ya Aamaleki, naononga konse konse anthu onse ndi
lupanga lakuthwa. 9Koma Sauli ndi anthu anamsunga wamoyo
Agagi, ndi nkhosa zokometsetsa, ndi ng'ombe, ndi zonenepa zina,
ndi ana a nkhosa, ndi zabwino zonse, sadafuna kuzitha psiti; koma
zonse zoipa ndi zonyansa anaziononga konse konse.

Samueli adzudzula Sauli pa kusamvera kwace

10Pamenepo mau a Yehova anafika kwa Samueli,
nati, 11Kundicititsa cisoni kuti ndinaika Sauli akhale mfumu; pakuti
wabwerera wosanditsata Ine, ndipo sanacita malamulo anga,
Ndipo Samueli anakwiya; nalira kwa Yehova usiku wonse. 12Ndipo
Samueli analawirira m'mawa kuti akakomane ndi Sauli; ndipo
munthu anamuuza Samueli kuti, Sauli anafika ku Karimeli, ndipo
taonani, anaimika cikumbutso cace, nazungulira, napitirira,
natsikira ku Giligala. 13Ndipo Samueli anadza kwa Sauli; ndipo
Sauli anati kwa iye, Yehova akudalitseni; ine ndinacita lamulo la
Yehova. 14Ndipo Samueli anati, Koma tsono kulirako kwa nkhosa
ndirikumva m'makutu anga, ndi kulirako kwa ng'ombe ndirikumva,
nciani? 15Ndipo Sauli anati, Anazitenga kwa Aamaleki; pakuti anthu
anasunga nkhosa zokometsetsa ndi ng'ombe, kuzipereka nsembe
kwa Yehova Mulungu wanu; koma zina tinaziononga konse
konse. 16Pomwepo Samueli ananena ndi Sauli, Imani,
ndidzakudziwitsani cimene Yehova wanena ndi ine usiku walero.
Ndipo iyeyo anati kwa iye, Nenani. 17Nati Samueli, M'mene munali
wamng'ono m'maso a inu nokha, kodi simunaikidwa mutu wa

mafuko a Israyeli? Ndipo Yehova anakudzozani mfumu ya Israyeli, 18Ndipo Yehova anakutumani ulendo, kuti, Muka, nuononge konse konse Aamaleki akucita zoipawo, nuponyane nao kufikira utawatha. 19Cifukwa ninji tsono simunamvera mau a Yehova, koma munathamangira zowawanya, ndi kucita coipa pamaso pa Yehova? 20Ndipo Sauli ananena ndi Samueli, Koma ndinamvera mau a Yehova, ndipo ndinayenda njira Yehova ananditumа ine, ndipo ndinabwera naye Agagi mfumu ya Amaleki, ndi Aamaleki ndinawaononga konse konse. 21Koma anthuwo anatengako zowawanya, nkhosa ndi ng'ombe, zoposa za zija tidayenera kuziononga, kuziphera nsembe kwa Yehova Mulungu wanu ku Giligala. 22Ndipo Samueli anati, Kodi Yehova akondwera ndi nsembe zopsereza ndi nsembe zophera, monga ndi kumvera mau a Yehova? Taonani, kumvera ndiko kokoma koposa nsembe, kuchera khutu koposa mafuta a nkhosa zamphongo, 23Pakuti kupanduka kuli ngati coipa ca kucita nyanga, ndi mtima waliuma uli ngati kupembedza milungu yacabe ndi maula. Popeza inu munakaniza mau a Yehova, Iyenso anakaniza inu, kuti simudzakhalanso mfumu. 24Ndipo Sauli anati kwa Samueli, Ndinacimwa; pakuti ndinalumpha lamulo la Yehova, ndi mau anu omwe; cifukwa ndinaopa anthuwo, ndi kumvera mau ao. 25Cifukwa cace tsono, mukhululukire cimo langa, nimubwerere pamodzi ndi ine, kuti ndikalambire Yehova. 26Ndipo Samueli ananena ndi Sauli, Ine sindibwerera nanu; pakuti munakaniza mau a Yehova, ndipo Yehova anakaniza inu, kuti simudzakhalanso mfumu ya Israyeli. 27Ndipo pakupotoloka Samueli kuti acoke, iye anagwira cilezi ca mwinjiro wace, ndipo cinang'ambika. 28Ndipo Samueli ananena naye, Yehova anang'amba ufumu wa Israyeli lero kuucotsa kwa inu, naupatsa kwa mnansi wanu wina wabwino woposa inu. 29Ndiponso Wamphamvu wa Israyeli sanama kapena kulapa; popeza iye sali munthu kuti akalapa. 30Pomwepo iye anati, Ndinacimwa, koma mundicitire ulemu tsopano pamaso pa akuru a anthu anga, ndi pamaso pa Israyeli, nimubwerere pamodzi ndi ine, kuti ndikalambire Yehova Mulungu wanu. 31Comweco Samueli anabwerera natsata Sauli; ndi Sauli analambira Yehova. 32Ndipo Samueli anati, Bwerani naye kwa ine kuno Agagi mfumu ya Aamaleki. Ndipo Agagi anabwera kwa iye mokondwera. Nati Agagi, Zoonadi kuwawa kwa imfa kunapitirira. 33Ndipo Samueli anati, Monga lupanga lako linacititsa akazi ufedwa, momwemo mai wako adzakhala mfedwa mwa akazi. Ndipo Samueli anamdula Agagi nthuli nthuli pamaso pa Yehova ku Giligala. 34Pamenepo Samueli ananka ku Rama; ndi Sauli anakwera kunka ku nyumba yace ku Gibeya wa Sauli. 35Ndipo Samueli sanadzanso kudzaona Sauli kufikira tsiku la imfa yace; koma Samueli analira

cifukwa ca Sauli; ndipo Yehova anali ndi cisoni kuti anamlonga Sauli mfumu ya Israyeli.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Samueli adzoza Davide akhale mfumu

1Ndipo Yehova ananena ndi Samueli, Iwe ukuti ulire cifukwa ca
Sauli nthawi yotani, popeza Ine ndinamkana kuti asakhale mfumu
ya Israyeli? Dzaza nyanga yako ndi mafuta, numuke,
ndidzakutumiza kwa Jese wa ku Betelehemu; pakuti ndinadzionera
mfumu pakati pa ana ace. 2Ndipo Samueli anati, Ndikamuka
bwanji? Sauli akacimva, adzandipha. Ndipo Yehova anati, Umuke
nayo ng'ombe yaikazi, nunene kuti, Ndadza kudzaphera nsembe
kwa Yehova. 3Ndipo uitane Jese abwere kunsembeko, ndipo Ine
ndidzakusonyeza cimene uyenera kucita; ndipo udzandidzozera iye
amene ndidzakuchulira dzina lace. 4Ndipo Samueli anacita cimene
Yehova ananena, nadza ku Betelehemu. Ndipo akuru a mudziwo
anadza kukomana naye monthunthumira, nati, Mubwera ndi
mtendere kodi? 5Nati iye, Ndi mtendere umene; ndadza
kudzaphera nsembe kwa Yehova; mudzipatule ndi kufika ndi ine
kunsembeko. Ndipo iye anapatula Jese ndi ana ace, nawaitanira
kunsembeko. 6Ndipo kunali, pakufika iwo, iye anayang'ana pa
Eliyabu, nati, Zoonadi, wodzozedwa wa Yehova ali pamaso
pace. 7Koma Yehova ananena ndi Samueli, Vsayang'ane nkhope
yace, kapena kutalika kwa msinkhu wace, popeza Ine ndinamkana
iye; pakuti Yehova saona monga aona munthu; pakuti munthu
ayang'ana cooneka ndi maso, koma Yehova ayang'ana
mumtima. 8Pamenepo Jese anaitana Abinadabu nampititsa pa
Samueli. Ndipo iye adati, Koma uyunso Yehova
sadamsankha. 9Pamenepo Jese anapititsapo Sama. Ndipo anati,
Koma uyunso Yehova sanamsankha. 10Ndipo Jese anapititsapo ana
ace amuna asanu ndi awiri. Koma Samueli anati kwa Jese, Yehova
sanawasankha awa. 11Ndipo Samueli anati kwa Jese, Ana anu ndi
omwewa kodi? Nati iye, Watsala wina, mng'ono wa onse, ndipo
taonani, iye alikuweta nkhosa. Ndipo Samueli anati kwa Jese,
Tumiza munthu akamtenge; pakuti ife sitidzakhala pansi kufikira
iye atadza kuno. 12Ndipo anatumiza munthu, nabwera naye. Tsono
iye anali wofiirira, ndi wa nkhope yokongola, ndi maonekedwe
okoma. Ndipo Yehova anati, Nyamuka umdzoze, pakuti ndi
ameneyu. 13Pamenepo Samueli anatenga nyanga ya mafuta,
namdzoza pakati pa abale ace; ndipo mzimu wa Yehova unalimbika
pa Davide kuyambira tsiku lomweli. Ndipo Samueli ananyamuka,
Danks ku Rama.

Davide atumikira Sauli

14Koma mzimu wa Yehova unamcokera Sauli, ndi mzimu woipa
wocokera kwa Yehova unambvuta iye. 15Ndipo anyamata a Sauli
ananena naye, Onani tsopano, mzimu woipa wocokera kwa
Mulungu ulikubvuta inu. 16Tsono inu mbuye wathu muuze

anyamata anu, amene ali pamaso panu, kuti afune munthu wanthetemya wodziwa kuyimba zeze; ndipo kudzakhala, pamene mzimu woipa wocokera kwa Mulungu uli pa inu, iyeyo adzayimba ndi dzanja lace, ndipo mudzakhala wolama. 17Ndipo Sauli anati kwa anyamata ace, Mundifunire tsono munthu wakudziwa kuyimba bwino, nimubwere naye kwa ine. 18Ndipo mnyamata wace wina anayankha, nati, Taonani, ine ndaona mwana wa Jese wa ku Betelehemu, ndiye wanthetemya wodziwa kuyimbira, ndipo ali wa mtima wolimba ndi woyenera nkhondo, ndiponso ali wocenjera manenedwe ace; ndiye munthu wokongola, ndipo Yehova ali naye. 19Cifukwa cace Sauli anatumiza mithenga kwa Jese, nati, Vnditumizire Davide, mwana wako, amene ali kunkhosa. 20Ndipo Jese anatenga buru namsenza mkate, ndi thumba la vinyo, ndi: mwana wa mbuzi, nazitumiza kwa Sauli ndi Davide mwana wace. 21Ndipo Davide anafika kwa Sauli, naima pamaso pace; ndipo iye anamkonda kwambiri, namsandutsa wonyamula zida zace. 22Ndipo Sauli anatumiza kwa Jese, nati, Ulole kuti Davide aime pamaso panga; pakuti ndamkomera mtima. 23Ndipo kunali kuti pamene mzimu woipawo wocokera kwa Mulungu unali pa Sauli, Davide anatenga zeze, naliza ndi dzanja lace; comweco Sauli anatsitsimuka, nakhala bwino, ndi mzimu woipa unamcokeraiye.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Davide apha Goliati

1Pamenepo Afilisti anasonkhanitsa makamu ao a nkhondo,
naunjikana ku Soko wa ku Yuda, namanga zithando pakati pa Soko
ndi Azeka ku Efesi-damimu. 2Ndipo Sauli ndi anthu a Israyeli
anasonkhana, namanga zithando pa cigwa ca Ela, nandandalitsa
nkhondo yao kuti akaponyane ndi Afilisti. 3Ndipo Afilisti anaima
paphiri tsidya lija, ndi Aisrayeli anaima paphiri tsidya lina; ndi
pakati pao panali cigwa. 4Ndipo ku zithando za Afilisti kunaturuka
ciwinda, dzina lace Goliate wa ku Gati, kutalika kwace ndiko
mikono isanu ndi umodzi ndi cikhato. 5Ndipo anali ndi cisoti
camkuwa pamutu pace, nabvala maraya aunyolo, olemera ngati
masekeli zikwi zisanu za mkuwa, 6nakuta msongolo wace ndi
cobvala camkuwa, ndiponso pacikota pace panali nthungo
yamkuwa. 7Ndipo mtengo wa mkondo wace unali ngati mtanda
woombera nsaru; ndi khali la mkondowo linalemera ngati masekeli
mazana asanu ndi limodzi a citsulo; ndipo womnyamulira cikopa
anamtsogolera. 8Naima iye naitana makamu a nkhondo a Israyeli,
nanena nao, Munaturukiranji kundandalitsa nkhondo yanu? Sindine
Mfilisti kodi, ndi inu anyamata a Sauli? mudzisankhire munthu,
atsikire kwa ine. 9Akakhoza iyeyo kuponyana ndi ine ndi kundipha,
tidzakhala ife akapolo anu; koma ine ndikamlaka, ndi kumupha,
tsono mudzakhala inu akapolo athu, ndi kutitumikira ife. 10Nati
Mfilistiyo, Ine ndinyoza makamu a nkhondo a Israyeli lero;
mundipatse munthu, kuti tilimbane ife awiri. 11Ndipo pamene Sauli
ndi Aisrayeli onse anamva mau ao a Mfilistiyo, anadodoma, naopa
kwambiri. 12Tsono Davide anali mwana wa M-efrati uja wa ku
Betelehemu-Yuda, dzina lace ndiye Jese; ameneyu anali nao ana
amuna asanu ndi atatu; ndipo m'masiku a Sauli munthuyo anali
nkhalamba, mwa anthu. 13Ndipo ana atatu akuru a Jese anatsata
Sauli kunkhondoko; ndi maina ao a ana ace atatuwo adapita ku
nkhondowo ndiwo Eliabu woyambayo, ndi mnzace womponda
pamutu pace Abinadabu, ndi wacitatu Sama. 14Ndipo Davide anali
wotsiriza; ndi akuru atatuwo anamtsata Sauli. 15Koma Davide
akamuka kwa Sauli, nabwerera kudzadyetsa nkhosa za atate wace
ku Betelehemu. 16Ndipo Mfilistiyo anayandikira m'mawa ndi
madzulo, nadzionetsera masiku makumi anai.
17Ndipo Jese anati kwa Davide mwana wace, Uwatengere abale
ako efa watirigu uyu wokazinga, ndi mikate iyi khumi,
nuthamangire nazo kuzithando kwa abale ako; 18nunyamule ncinci
izi khumi zamase ukapatse mtsogoleri wa cikwi cao, nukaone
m'mene akhalira abale ako, nulandire cikole cao, 19Tsono Sauli, ndi
iwowa, ndi anthu onse a Israyeli, anali m'cigwa ca Ela, ku nkhondo
ya Afilisti. 20Ndipo Davide anauka m'mamawa, nasiyira nkhosa

wozisungira, nasenza zija, namuka, monga anamuuza Jese; ndipo iye anafika ku linga la magareta, napeza khamu lirikuturuka kunka poponyanira nkhondo lirikupfuula. 21Ndipo Israyeli ndi Afilisti anandandalitsa nkhondo zao, khamu tina kuyang'anana ndi khamu lina. 22Ndipo Davide anasiya akatundu ace m'dzanja la wosungira akatundu, nathamangira ku khamulo, nadza nalankhula abale ace. 23Ndipo m'mene iye anali cilankhulire nao, onani cinakwerako ciwindaco, Mfilisti wa ku Gati, dzina lace ndiye Goliate, woturuka pakati pa mipambo ya Afilisti, nalankhula monga mau omwe aja; ndipo Davide anawamva. 24Ndipo Aisrayeli onse, pakumuona munthuyo, anamthawa, naopa kwambiri. 25Nati Aisrayeli, Kodi mwaona munthu uyu amene anakwera kuno? zoonadi iye anakwera kuti adzanyoze Israyeli, ndipo munthu wakumupha iye, mfumu idzamlemeza ndi cuma cambiri, nidzampatsa mwana wace wamkazi, nidzayesa nyumba ya atate wace yaufulu m'Israyeli. 26Ndipo Davide analankhula ndi anthu akuima pafupi ndi iye, nati, Adzamcitira ciani munthu wakupha Mfilisti uyu, ndi kucotsa tonzo lace pakati pa Israyeli? pakuti Mfilisti uyu wosadulidwa ndiye yani, kuti azinyoza makamu a Mulungu wamoyo? 27Ndipo anthuwo anamyankha motero, nati, Adzamcitira munthu wakumupha iye mwakuti mwakuti. 28Ndipo Eliabu mkuru wace anamumva iye alikulankhula ndi anthu; ndipo Eliabu anapsa mtima ndi Davide, nati, Unatsikiranji kuno? ndi nkhosa zija zowerengeka unazisiya ndi yani, m'cipululu muja? Ine ndidziwa kudzikuza kwako ndi kuipa kwa mtima wako; pakuti watsika kuti udzaone nkhondoyi. 29Ndipo Davide anati, Ndacitanji tsopano? Palibe cifukwa kodi? 30Napotolokera iye kwa munthu wina, nalankhula mau omwewo; ndipo anthu anamyankhanso monga momwemo. 31Ndipo pamene mau adanena Davide anamveka, anawapitiriza kwa Sauli; ndipo iye anamuitana. 32Ndipo Davide anati kwa Sauli, Asade nkhawa munthu ali yense cifukwa ca iyeyo; ine kapolo wanu ndidzapita kuponyana ndi Mfilisti uyu. 33Ndipo Sauli anati kwa Davide, Sukhoza iwe kukomana ndi Mfilisti uyu kukaponyana naye; pakuti iwe ndiwe mnyamata, koma iye anazolowera nkhondo kuyambira ubwana wace. 34Ndipo Davide anati kwa Sauli, Ine kapolo wanu ndinalikusunga nkhosa za atate wanga; ndipo pakubwera mkango, mwina cimbalangondo ndi kutenga nkhosa ya gululo, 35ndinacithamangira, ndi kucikantha, ndi kuiturutsa m'kamwa mwace; ndipo pamene cinaneliukira, ndinagwira cowa lace ndi kucikantha ndi kucipha. 36Ine kapolo wanu ndinapha mkango ndi cimbalangondo zonse ziwiri; ndipo Mfilisti uyu wosadulidwa adzakhala ngati mmodzi wa izo, popeza wanyoza makamu a Mulungu wamoyo. 37Nati Davide, Yehova wakundipulumutsa pa mphamvu ya mkango, ndi mphamvu ya

cimbalangondo, Iyeyu adzandipulumutsa m'dzanja la Mfilisti uyu, Ndipo Sauli anati kwa Davide, Muka, Yehova akhale nawe. 38Ndipo Sauli anabveka Davide zobvala zace za iye yekha, nambveka cisoti camkuwa pamutu pace, nambvekanso maraya aunyolo. 39Ndipo Davide anamanga lupanga lace pamwamba pa zobvala zace, nayesa kuyenda nazo; popeza sanaziyesera kale. Ndipo Davide anati kwa Sauli, Sindikhoza kuyenda ndi izi; pakuti sindinazizolowera. Nazibvula Davide. 40Natenga ndodo yace m'dzanja lace nadzisankhira miyala isanu yosalala ya mumtsinje, naiika m'thumba la kubusa, limene anali nalo ndilo cibete; ndi coponyera miyala cinali m'dzanja lace, momwemo anayandikira kwa Mfilistiyo. 41Ndipo Mfilistiyo anadza, nayandikira kwa Davide; ndi wonyamula cikopa cace anamtsogolera. 42Ndipo Mfilisti pakumwazamwaza maso, ndi kuona Davide, anampeputsa; popeza anali mnyamata cabe, wofiirira, ndi wa nkhope yokongola. 43Ndipo Mfilisti anati kwa Davide, Ine ndine garu kodi, kuti iwe ukudza kwa ine ndi ndodo? Ndi Mfilistiyo anatukwana Davide nachula milungu yace. 44Ndipo Mfilistiyo anati kwa Davide, Idza kuno kwa ine, ndidzapatsa mnofu wako kwa mbalame za mlengalenga, ndi kwa zirombo za kuthengo. 45Ndipo Davide anati kwa Mfilistiyo, Iwe ukudza kwa ine ndi lupanga, ndi mkondo, ndi nthungo; koma ine ndafika kwa iwe m'dzina la Yehova wa makamu, Mulungu wa ankhondo a Israyeli amene iwe unawanyoza. 46Lero lino Yehova adzakupereka iwe m'dzanja langa, ndipo ndidzakukantha, ndi kukucotsera mutu wako. Ndipo lero ndidzapatsa mitembo ya makamu a Afilisti kwa mbalame za mlengalenga, ndi kwa zirombo za dziko lapansi; kuti dziko lonse likazindikire kuti kwa Israyeli kuli Mulungu. 47Ndi msonkhano wonse uno udzazindikira kuti Yehova sapulumutsa ndi lupanga, kapena ndi mkondo; pakuti Yehova ndiye mwini nkhondo, ndipo iye adzakuperekani inu m'manja athu. 48Ndipo kunali, pamene Mfilistiyo anadzikonza, nadza, nasendera pafupi kuti akomane ndi Davide, Davide anafulumira, nathamangira ku khamulo, kuti akomane ndi Mfilistiyo. 49Ndipo Davide anapisa dzanja lace m'thumba mwace, naturutsamo mwala, nauponya, nalasa Mfilistiyo pamphumi; ndi mwalawo unalowa m'mphumi, ndipo iye anagwa pansi cafufumimba. 50Comweco Davide anapambana Mfilistiyo ndi mwala wa coponyera cace, nakantha Mfilistiyo, namupha. Koma m'dzanja la Davide munalibe lupanga. 51Potero Davide anathamanga naima pa Mfilistiyo, nagwira lupanga lace, nalisolola m'cimace, namtsiriza nadula nalo mutu wace. Ndipo pakuona Afilisti kuti ciwinda cao cidafa, anathawa. 52Ndipo anthu a Israyeli ndi Ayuda ananyamuka, napfuula, nathamangira Afilistiwo, mpaka ufika kucigwako, ndi ku zipata za Ekroni. Ndipo Afilistiwo olasidwa

anagwa pa njira ya ku Saraimu, kufikira ku Gad ndi ku
Ekroni. 53Ndipo ana a Israyeli atathamangira Afilisti, anabwerera
nafunkha za m'zithando zao. 54Ndipo Davide anatenga mutu wa
Mfilistiyo, napita nao ku Yerusalemu; koma zida zace anazisunga
m'hema wace.
55Ndipo pamene Sauli anaona Davide alikuturukira kwa Mfilistiyo,
iye anati kwa Abineri, kazembe wa khamu la nkhondo, Abineri,
mnyamata uyu ndi mwana wa yani? Nati Abineri, Pali moyo wanu,
mfumu, ngati ndidziwa. 56Ndipo mfumu inati, Ufunsire kuti
mnyamatayo ndi mwana wa yani. 57Ndipo pamene Davide
anabwera, atapha Mfilistiyo, Abineri anamtenga, nafika naye
pamaso pa Sauli, mutu wa Mfilistiyo uli m'dzanja lace. 58Ndipo
Sauli anati kwa iye, Mnyamata iwe, ndiwe mwana wa yani? Davide
nayankha, Ndiri mwana wa kapolo wanu Jese wa ku Betelehemu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Ubwenzi wa Davide ndi Jonatani

1Ndipo kunali, pakutsiriza iye kulankhula ndi Sauli, mtima wa
Jonatani unalumikizika ndi mtima wa Davide, ndipo Jonatani
anamkonda iye monga moyo wa iye yekha. 2Ndipo Sauli
anamtenga tsiku lomwelo, osamlolanso apite kwao kwa atate
wace. 3Pamenepo Jonatani ndi Davide anapangana pangano,
pakuti adamkonda iye ngati moyo wa iye yekha. 4Ndipo Jonatani
anabvula maraya ace anali nao, napatsa Davide, ndi zobvala zace,
ngakhale lupanga lace, ndi uta wace, ndi lamba lace. 5Ndipo
Davide anaturuka kunka kuli konse Sauli anamtumako, nakhala
wocenjera; ndipo Sauli anamuika akhale woyang'anira anthu a
nkhondo; ndipo ici cinakomera anthu onse, ndi anyamata a Sauli
omwe.
6Ndipo kunali pakudza iwo, pamene Davide anabwera atapha
Afilistiwo, anthu akazi anaturuka m'midzi yonse ya Israyeli, ndi
kuyimba ndi kubvina, kuti akakomane ndi mfumu Sauli, ndi
malingaka, ndi cimwemwe, ndi zoyimbira. 7Ndipo akazi
anathirirana mang'ombe m'kuyimba kwao, nati,
Sauli anapha zikwi zace,
Koma Davide zikwi zace zankhani.

Sauli aipidwa ndi Davide

8Koma Sauli anakwiya ndithu, ndi kunenaku kunamuipira; nati, Kwa
Davide anawereogera zikwi zankhani, koma kwa ine zikwi zokha;
cimperewera ncianioso, koma ufumu wokha? 9Ndipo kuyambira
tsiku lomwelo ndi m'tsogolo mwace, Sauli anakhala maso pa
Davide.
10Ndipo kunali m'mawa mwace, mzimu woipa wocokera kwa
Mulungu unamgwira Sauli mwamphamvu, iye nalankhula
moyaruka m'nyumba yace; koma Davide anayimba ndi dzanja
lace, monga amacita tsiku ndi tsiku; koma m'dzanja la Sauli munali
mkondo. 11Ndipo Sauli anaponya mkondowo; pakuti anati,
Ndidzapyoza Davide ndi kumphatikiza ndi khoma. Ndipo Davide
analewa kawiri kucoka pamaso pace. 12Ndipo Sauli anaopa Davide,
cifukwa Yehova anali naye, koma adamcokera Sauli. 13Cifukwa
cace Sauli anamcotsa kuti asakhale naye, namuika akhale
mtsogoleri wace wa anthu cikwi cimodzi; ndipo iye anatsogolera
anthu kuturuka ndi kubwera nao. 14Ndipo Davide anakhala
wocenjera m'mayendedwe ace onse; ndipo Yehova anali
naye. 15Ndipo pamene Sauli anaona kuti analikukhala wocenjera
ndithu anamuopa. 16Koma Aisrayeli onse ndi Ayuda onse
anamkonda Davide pakuti anawatsogolera kuturuka ndi kulowa
nao.

Davide mkamwini wa Sauli

17Ndipo Sauli anati kwa Davide, Ona, mwana wanga wamkazi
wamkuru, dzina lace Merabi, iyeyo ndidzakupatsa akhale mkazi
wako; koma undikhalire ngwazi, nuponye nkhondo za Yehova.
Pakuti Sauli anati, Dzanja langa lisamkhudze, koma dzanja la
Afilisti ndilo. 18Ndipo Davide anati kwa Sauli, Ine ndine yani, ndi
moyo wanga uli wotani, kapena banja la atate wanga liri lotani
m'Israyeli, kuti ine ndidzakhala mkamwini wa mfumu? 19Koma
kunali nthawi imene akadapatsa Merabi mwana wamkazi wa Sauli
kwa Davide, iye anapatsidwa kwa Adrieli Mholati kukhala mkazi
wace. 20Ndipo Mikala mwana wamkazi wa Sauli anakonda Davide;
ndipo pakumva Sauli, anakondwera nako. 21Nati Sauli,
Ndidzampatsa iye, kuti amkhalire msampha, ndi kuti dzanja la
Afilisti limgwere. Cifukwa cace Sauli ananena ndi Davide, Lero
udzakhala mkamwini wanga kaciwiri. 22Ndipo Sauli analamulira
anyamata ace, nati, Mulankhule naye Davide m'tseri, ndi kuti,
Taonani mfumu akondwera nanu, ndi anyamata ace onse
akukondani; cifukwa cace tsono, khalani mkamwini wa
mfumu. 23Ndipo anyamata a Sauli analankhula mau awa m'makutu
a Davide. Nati Davide, Kodi muciyesera cinthu copepuka kukhala
mkamwini wa mfumu, popeza ndiri munthu wosauka, ndi
wopeputsidwa. 24Ndipo anyamata a Sauli anamuuza, kuti, Anatero
Davide. 25Nati Sauli, Mudzatero kwa Davide, kuti mfumu safuna
colowolera cina, koma nsonga za makungu zana limodzi za Afilisti,
kuti abwezere cilango adani a mfumu. Koma Sauli anaganizira
kupha Davide ndi dzanja la Afilisti. 26Ndipo pamene anyamata ace
anauza Davide mau awa, kudamkomera Davide kukhala mkamwini
wa mfumu. 27Ndipo asanathe masikuwo, ananyamuka Davide, ndi
anthu ace, nakaphako Afilisti mazana awiri, ndipo Davide anatenga
nsonga za makungu ao nazipatsa mofikira kwa mfumu, kuti akhale
mkamwini wa mfumu. Ndipo Sauli anampatsa Mikala mwana wace
wamkazi akhale mkazi wace. 28Ndipo Sauli anaona, nadziwa kuti
Yehova ali ndi Davide; ndi kuti Mikala mwana wa Sauli anamkonda
Davide. 29Sauli nayamba kumuopa Davide kopambana; ndi Sauli
anali mdani wa Davide masiku onse.
30Pomwepo mafumu a Afilisti anaturuka; ndipo nthawi zonse
anaturuka iwo, Davide anali wocenjera koposa anyamata onse a
Sauli, comweco dzina lace linatamidwa kwambiri.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Jonatani anenera Davide kwa Sauli

1Ndipo Sauli analankhula kwa Jonatani mwana wace, ndi anyamata
ace onse kuti amuphe Davide. 2Koma Jonatani mwana wa Sauli
anakondwera kwambiri ndi Davide. Ndipo Jonatani anauza Davide,
nati, Sauli atate wanga alikufuna kukupha; cifukwa cace tsono
ucenjere m'mawa, mukhale m'malo mosadziwika, nubisale; 3ndipo
ine ndidzaturuka ndi kuima pa mbali ya atate wanga kumunda
kumene kuli iwe, ndipo ndidzalankhula ndi atate wanga za iwe;
ndipo ndikaona kanthu ndidzakudziwitsa. 4Ndipo Jonatani
analankhula ndi atate wace mobvomereza Davide, nanena naye,
Mfumu asacimwire mnyamata wace Davide; cifukwa iyeyo
sanacimwira inu, ndipo nchito zace anakucitirani zinali zabwino
ndithu; 5popeza iye anataya moyo wace nakantha Mfilistiyo, ndipo
Yehova anacitira Aisrayeli onse cipulumutso cacikuru, inu
munaciona, nimnnakondwera; tsono mudzacimwiranji mwazi
wosalakwa, ndi kumupha Davide popanda cifukwa? 6Ndipo Sauli
anamvera mau a Jonatani; nalumbira, Pali Yehova, sadzaphedwa
iye. 7Pamenepo Jonatani anaitana Davide, namuuza zonsezi. Ndipo
Jonatani anafika naye Davide kwa Sauli, iye nakhalanso pamaso
pace monga kale.

Sauli ajuna kupha Davide, Mikala ampulumutsa

8Ndipo kunalinso nkhondo; ndipo Davide anaturuka, nakamenyana
ndi Afilisti, nawapha ndi maphedwe akuru, ndipo iwo anamthawa
iye. 9Ndipo mzimu woipa wocokera kwa Yehova unali pa Sauli,
pakukhala iye m'nyumba mwace, ndi mkondo wace m'dzanja lace;
ndipo Davide anayimba ndi dzanja lace. 10Ndipo Sauli anayesa
kupyoza Davide kumphatikiza kukhoma ndi mkondowo; koma iye
anadzilanditsa kucoka pamaso pa Sauli; ndipo analasa khoma;
ndipo Davide anathawa napulumuka usiku uja. 11Ndipo Sauli
anatumiza mithenga ku nyumba ya Davide imdikire, ndi kumupha
m'mawa; koma Mikala mkazi wa Davide anamuuza, nati, Ukapanda
kupulumutsa moyo wako usiku uno, udzaphedwa ndithu
m'mawa. 12Comweco Mikala anamtsitsira Davide pazenera,
namuka iye, nathawa, napulumuka. 13Ndipo Mikala anatenga
cifanizo naciika pakama, naika mtsamiro wa ubweya wa mbuzi
kumutu kwace, nacipfunda zopfunda. 14Ndipo pamene Sauli
anatumiza mithenga kuti ikamgwire Davide, anati, iye
alikudwala. 15Ndipo Sauli anatumiza mithengayo kuti ikaone
Davide, nati, Mumtengere iye pa kama wace, kuti
ndidzamuphe. 16Ndipopakulowamithengayo, onani, pakama pali
cifanizo ndi mtsamiro wa ubweya wa mbuzi kumutu kwace. 17Nati
Sauli kwa Mikala, Wandinyengeranii comweci, ndi kulola mdani

wanga apulumuke? Ndipo Mikala anayankha Sauli, iye anati kwa ine, Undilole ndipite, ndingakuphe.

Sauli ndi amithenga ace anenera

18Comweco anathawa Davide, napulumuka, nafika kwa Samueli: ku Rama, namuuza zonse Sauli anamcitira. Ndipo iye ndi Samueli anakhala ku Nayoti. 19Ndipo wina anauza Sauli, kuti, Onani Davide ali ku Nayoti m'Rama. 20Ndipo Sauli anatumiza mithenga kuti igwire Davide, ndipo pamene inaona gulu la aneneri alikunenera, ndi Samueli mkuru wao alikuimapo, mzimu wa Mulungu unagwera-mithenga ya Sauli, ninenera iyonso. 21Ndipo pamene anauza Sauli, iye anatumiza mithenga yina; koma iyonso inanenera. Ndipo Sauli anatumiza mithenga kacitatu, nayonso inanenera. 22Pamenepo iyenso anamuka ku Rama, nafika ku citsime cacikuru ciri ku Seku, nafunsa Dati, Samueli ndi Davide ali kuti? Ndipo wina anati, Taonani, ali ku Nayoti m'Rama. 23Ndipo anapita komweko ku Nayoti m'Rama; ndi mzimu wa Mulungu unamgwera iyenso; ndipo anapitirira, nanenera, mpaka anafika ku Nayoti m'Rama. 24Ndiponso anabvula zobvala zace, naneneranso pamaso pa Samueli nagona wamarisece usana womwe wonse, ndi usiku womwe wonse. Cifukwa cace amati, Kodi Saulinso ali pakati pa aneneri?

©The Bible Society of Malawi, 1992

Pangano pakati pa Davide ndi Jonatani

1Ndipo Davide anathawa ku Nayoti m'Rama, nadzanena pamaso
pa Jonatani, Ndacitanji ine? kuipa kwanga kuli kotani? ndi chimo
langa la pamaso pa atate wanu ndi ciani, kuti amafuna moyo
wanga? 2Namyankha, Usatero iai, sudzafa; ona, atate, wanga
sacita kanthu kakakuru kapena kakang'ono wosandidziwitsa ine;
atate wanga adzandibisiranji cinthu cimeneci? Si kutero ai. 3Ndipo
Davide analumbiranso nati, Atate wako adziwatu kuti wandikomera
mtima; nati, Jonatani asadziwe ici, kuti angamve cisoni; koma pali
Yehova, ndiponso pali moyo wako, pakati pa ine ndi imfa pali ngati
phazilimodzi. 4Ndipo Jonatani anati kwa Davide, Ciri conse mtima
wako unena, ndidzakucitira. 5Nati Davide kwa Jonatani, Onani,
mawa mwezi ukhala, ndipo ine ndiyenera kupita kukadya kwa
mfumu, wosatsala; koma undilole ndikabisale kuthengo, kufikira
tsiku lacitatu madzulo ace. 6Atate wako akandifuna pang'ono
ponse, unene kuti, Davide anandiumirira ndimlole athamangire
kwao ku Betelehemu, pakuti kumeneko kuli nsembe ya pacaka ya
banja lao lonse. 7Tsono akati, Cabwino; kapolo wako adzakhala ndi
mtendere; koma akapsa mtima, uzindikirepo kuti anatsimikiza
mtima kundicitira coipa. 8Cifukwa cace ucitire kapolo wako zokoma
mtima; popeza wamcititsa kapolo wako kupangana nawe pangano
la kwa Yehova; koma ngati mwa ine muli coipa ciri conse, undiphe
wekha; udzapita nane bwanji kwa atate wako? 9Ndipo Jonatani
anati, lai ndi pang'ono ponse; ine ndikadziwa konse kuti atate
wanga anatsimikiza mtima kukucitira coipa, sindidzadziwitsa iwe
kodi? 10Tsono Davide anati kwa Jonatani, Adzandiuza ndani ngati
atate wako alankhulira iwe mokalipa? 11Nati Jonatani kwa Davide,
Tiyeni timuke kuthengo. Namuka onse awiri kuthengoko.
12Ndipo Jonatani anati kwa Davide, Yehova, Mulungu wa Israyeli,
akhale mboni; nditaphera mwambi atate wanga mawa dzuwa lino,
kapena mkuca, onani, pakakhala kanthu kabwino kakucitira
Davide, sindidzakutumira mthenga ndi kukuululira kodi? 13Mulungu
alange Jonatani, ndi kuonjezapo, ngati atate wanga akondwera
kukucitira coipa, ine osakuululira, ndi kukucotsa kuti upite
mumtendere; ndipo Yehova akhale nawe, monga anakhala naye
atate wanga. 14Ndipo undionetsere cifundo ca Yehova, si pokhala
ine ndi moyo pokha, kuti ndingafe; 15komanso usaleke kucitira
cifundo a m'nyumba yanga nthawi zonse; mungakhale
m'tsogolomo Yehova atathera adani onse a Da vide pa dziko
lapansi. 16Comweco Jonatani anapangana pangano ndi nyumba ya
Davide, ndipo Yehova anakwaniritsa izi polanga adani a
Davide. 17Ndipo Jonatani anamlumbiritsa Davide kaciwiri, cifukwa
anamkonda; popeza anamkonda monga anakonda moyo wa iye

yekha. 18Tsono Jonatani ananena kwa Davide, Mawa mwezi ukhala;
ndipo adzakufuna, popeza udzasoweka pamalo pako. 19Ndipo
atapita masiku atatu, utsike msanga, nufike kumene unabisala
tsiku la mrandu uja, nukhale pa mwala wa Ezeri. 20Ndipo ine
ndidzaponya mibvi itatu pambali pace, monga ngati ndirikuponya
pacandamali. 21Ndipo taona, ndidzatumiza mnyamatayo, ndi kuti,
Kafune mibviyo, Ndikamuuza mwanayo, kuti, Taona mibvi iri
cakuno; uitole nubwere, popeza pali mtendere kwa iwe, palibe
kanthu, pali Yehova. 22Koma ndikati kwa mnyamatayo, Ona mibvi
iri kutsogoloko; pamenepo unyamuke ulendo wako; popeza Yehova
wakuuza umuke. 23Ndipo za cija tinakambirana iwe ndi ine, taona,
Yehova ali pakati pa ife nthawi zonse.
24Comweco Davide anabisala kuthengo; ndipo pakukhala mwezi,
mfumu inakhala pansi kudya. 25Mfumu nikhala pa mpando wace,
monga adafocita nthawi zina, pa mpando wa pafupi pa khoma.
Ndipo Jonatani anaimirira, ndi Abineri anakhala pa mbali ya Sauli;
koma Davide anasoweka pamalo pace. 26Koma Sauli sananena
kanthu tsiku lomwelo; cifukwa anaganizira, Kanthu kanamgwera
iye, ali wodetsedwa; indedi ali wodetsedwa. 27Ndipo kunali tsiku
laciwiri mwezi utakhala, Davide adasowekanso pamalo pace; ndipo
Sauli anati kwa Jonatani mwana wace, Mwana wa Jese walekeranji
kubwera kudya dzulo ndi lero lomwe? 28Ndipo Jonatani anayankha
Sauli, Davide anandiumiriza ndimlole amuke ku
Betelehemu; 29nati, Ndiloleni, ndimuke; cifukwa banja lathu
lipereka nsembe m'mudzimo; ndi mbale wanga anandiuzitsa
ndifikeko; tsono ngati wandikomera mtima undilole ndicoke,
ndikaone abale anga. Cifukwa ca ici safika ku gome la mfumu.

Sauli aipidwa ndi Jonatani

30Pamenepo Sauli anapsa mtima ndi Jonatani, nanena naye, Iwe
mwana wa mkazi wa matsutso ndi wopikisana, sindidziwa kodi kuti
wasankha mwana wa Jeseyo kudzinyaza wekha, ndi usiwa wa mai
wako yemwe? 31Popeza nthawi yonse mwana wa Jeseyo akhala ndi
moyo padziko, koma sudzakhazikika iwe, kapena ufumu wako.
Cifukwa cace tumiza tsopano numtengere kuno kwa ine, popeza
adzafa ndithu, 32Ndipo Jonatani anayankha Sauli atate wace,
nanena, Aphedwe cifukwa ninji? anacitanji? 33Ndipo Sauli
anamponyera mkondo kuti amgwaze; momwemo Jonatani
anazindikira kuti atate wace anatsimikiza mtima kupha
Davide. 34Pamenepo Jonatani anauka pagome wolunda ndithu,
osadya kanthu tsiku laciwiri la mwezi, pakuti mtima wace unali ndi
cisoni cifukwa ca Davide, popeza atate wace anamcititsa manyazi.

Davide ndi Jonatani alekana

35Ndipo m'mawa, Jonatani ananka kuthengoko pa nthawi imene
anapangana ndi Davide, ali ndi kamnayamata. 36Ndipo anauza

mnyamata waceyo, Thamanga uzikatola mibvi Imene ndidzaponya; ndipo analikuthamanga mnyamatayu, iye anaponya mubvi kuutumphitsa iye. 37Ndipo mnyamatayo atafika pa malo a mubvi umene Jonatani anauponya, Jonatani anapfuulira mnyamatayo, nati, Mubviwo suli m'tsogolo mwako kodi? 38Ndipo Jonatani anapfuulira mnyamatayo, nati, Yendesa, fulumira, usaima. Ndi mnyamata wa Jonatani anatola mibvi, nafika kwa mbuye wace. 39Koma mnyamatayo sanadziwa kanthu; Davide ndi Jonatani okha anadziwa za mranduwoo. 40Ndipo Jonatani anapatsa mnyamata wace zida zace, nanena naye, Muka, tenga izi kunka nazo kumudzi. 41Pomwepo pocoka mnyamatayo, Davide anauka cakumwera, nagwa nkhope yace pansi, nawerama katatu; ndipo iwowa anapsompsonana, nalirirana, kufikira Davide analiritsa. 42Ndipo Jonatani ananena kwa Davide, Muka mumtendere, popeza tonsefe tinalumbira m'dzina la Yehova, kuti, Yehova adzakhala pakati pa ine ndi iwe, ndi pakati pa mbeu yanga ndi mbeu yako, nthawi zamuyaya. 43Ndipo iye ananyamuka nacoka; koma Jonatani anamuka kumudzi.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Davide athawira kwa wansembe Ahimeleki ku Nobi

1Ndipo Davide anafika ku Nobi kwa! Ahimeleki wansembeyo; ndipo
Ahimeleki anadza kukomana ndi Davide alikunjenjemera, nanena
naye, Muli nokha bwanji, palibe munthu wina nanu? 2Nati Davide
kwa Ahimeleki wansembeyo, Mfumu inandilamulira nchito, ninena
nane, Asadziwe munthu ali yense kanthu za nchito imene
ndakutumira ndi kukulamulira; ndipo ndawapanga anyamatawo ku
malo akuti. 3Cifukwa cace tsono muli ndi ciani? mundipatse
m'dzanja langa mikate isanu, kapena ciri conse muli naco. 4Ndipo
wansembeyo anayankha Davide nati, Ndiribe mkate wacabe, koma
ulipo mkate wopatulika; pokhapo ngati anyamatawo anadzisunga
kupewa akazi. 5Ndipo Davide anayankha wansembeyo, nati naye,
Zoonadi tinafulatira akazi monga masiku atatu; cicokere ine,
zotengera za anayamatawo zinali zopatulika ungakhale unali
ulendo wacabe; koposa kotani nanga zotengera zao zikhala zoyera
lero? 6Comweco wansembeyo anampatsa mkate wopatulika,
popeza panalibe mkate wina, koma mkate woonekera, umene
adaucotsa pamaso pa Yehova, kuti akaike mkate wotentha tsiku
lomwelo anacotsa winawo. 7Tsono munthu wina wa anyamata a
Sauli anali komweko, tsiku lija, anacedwetsedwa pamaso pa
Yehova; dzina lace ndiye Doegi wa ku Edomu, kapitao wa abusa a
Sauli. 8Ndipo Davide ananena ndi Ahimeleki, Nanga pano m'dzanja
mwanu mulibe mkondo kapena lupanga kodi? cifukwa ine
sindinatenge lupanga langa kapena zida zanga, popeza mrandu wa
mfumu ukuti ndifulumire. 9Nati wansembeyo, Lupanga la Goliate
Mfilisti munamuphayo m'cigwa ca Ela, onani-liripo lokulunga
m'nsaru, kumbuyo kwa efodi; mukafuna kutenga limenelo,
tengani; popeza pano palibe lina, Ndipo Davide anati, Palibe lina
lotere longa lijalo, ndipatseni.

Davide athawira kwa Akisi

10Ndipo Davide ananyamuka, nathawa tsiku lomwelo cifukwa ca
kuopa Sauli, namuka kwa Akisi mfumu ya ku Gati. 11Ndipo
anyamata a Akisi ananena naye, Uyu si Davide mfumu ya dzikolo
kodi? Sanathirirana mang'ombe za iye kodi m'magule ao, ndi kuti,
Sauli anapha zikwi zace,
Koma Davide zikwi zace zankhani?
12Ndipo Davide anasunga mau awa mumtima mwace, naopa
kwambiri Akisi mfumu ya Gati. 13Nasanduliza makhalidwe ace
pamaso pao, nadzionetsera m'manja mwao ngati wamisala,
nangolembalemba pa zitseko za cipata, nakhetsa dobvu lace pa
ndebvu yace. 14Tsono Akisi ananena ndi anyamata ace, Taonani,
mupenya kuti munthuyo ngwa misala; mwabwera naye kwa ine
cifukwa ninji? 15Kodi ndisowa anthu amisala kuti mwabwera ndi uyu

kuti akhale wamisala pamaso panga? Kodi uyu adzalowa m'nyumba mwanga?

©The Bible Society of Malawi, 1992

Davide apulumukira ku phanga La Adulamu

1Motero Davide anacoka kumeneko, napulumukira ku phanga la ku
Adulamu; ndipo pamene abale ace ndi banja lonse la atate wace
anamva, iwo anatsikira kumeneko kwa iye. 2Ndipo yense
wosautsidwa, ndi yense wa ngongole, ndi yense wowawidwa
mtima, anaunjikana kwa iye; iye nakhala mtsogoleri wao; ndipo
anali nao anthu ngati mazana anai.
3Ndipo Davide anacoka kumeneko kunka ku Mizipa wa ku Moabu;
nati kwa mfumu ya Moabu, Mulole atate wanga ndi mai wanga
aturuke nakhale nanu, kufikira ndidziwa cimene Mulungu
adzandidtira. 4Ndipo anawatenga kumka nao pamaso pa mfumu ya
Moabu; ndipo iwo anakhala naye nthawi yonse Davide anali ku
lingalo. 5Ndipo mneneri Gadi anati kwa Davide, Musamakhala
m'lingamo; cokani, mulowe m'dziko la Yuda. Potero Davide
anacokako, nafika ku nkhalango ya Hereti.

Sauli aphetsa ansembe ndi onse ena a ku Nobi

6Pakumva Sauli kuti anadziwika Davide, ndi anthu ace akukhala
naye, Sauti analikukhala m'Gibeya, patsinde pa mtengo wa
kumsanje, m'dzanja lace munali mkondo wace, ndi anyamata ace
onse anaimirira pali iye. 7Ndipo Sauli anati kwa anyamata ace
akuima comzinga, Imvani tsopano, inu a Benjamini; kodi mwana
wa Jese adzakupatsani inu nonse minda, ndi minda yamphesa, kodi
adzakuikani mukhale atsogoleri a zikwi ndi a mazana; 8kuti inu
nonse munapangana dwembu pa ine, ndipo palibe wina
wakundiululira kuti mwana wanga anapangana pangano ndi
mwana wa Jese, ndipo palibe wilia wa inu wakundidtira cifundo
kapena kundidziwitsa kuti mwana wanga anafulumiza mnyamata
wanga kundilalira monga lero lomwe? 9Pamenepo Doegi wa ku
Edomu, anaimirira ndi anyamata a Sauli, nayankha, nati, Ine
ndinamuona mwana wa Jeseyo alikufika ku Nobi, kwa Ahimeleki
mwana wa Ahitubu. 10Ndipo iye anamfunsira kwa Yehova,
nampatsa cakudya, nampatsanso lupanga la Gotiate
Mfilistiyo. 11Pamenepo mfumu anatuma mthenga kukaitana
Ahimeleki wansembeyo, mwana wa Ahitubu, ndi banja lonse la
atate wace, ansembe a ku Nobi; ndipo iwo onse anafika kwa
mfumu. 12Ndipo Sauli anati, Imva tsopano iwe mwana wa Ahitubu.
Nayankha iye, Ndine, mbuye wanga. 13Ndipo Sauli anati kwa iye,
Munapangana dwembu pa ine bwanji, iwe ndi mwana wa Jese, kuti
unampatsa iye mkate, ndi lupanga, ndi kumfunsira kwa Mulungu
kuti iye andiukire, kundilalira, monga lero lomwe? 14Ndipo
Ahimeleki anayankha mfumu, nati, Ndipo ndani mwa anyamata
anu onse ali wokhulupirika ngati Davide amene, mkamwini wa
mfumu; wakuyenda mu uphungu wanu, nalemekezeka m'nyumba

mwanu? 15Kodi ndayamba lero kumfunsira kwa Mulungu? Musatero
iai; mfumu asanenera mnyamata wace kanthu, kapena nyumba
yonse ya atate wanga; popeza ine mnyamata wanu sindidziwa
kanthu ka izi zonse, ndi pang'ono ponse. 16Ndipo mfumu inati,
Ukufa ndithu Ahimeleki, iwe ndi banja lonse la atate
wako. 17Mfumu niuza asilikari akuima comzinga iye, Potolokani,
iphani ansembe a Yehova; cifukwa agwirizana ndi Davide, ndipo
anadziwa kuti alinkuthawa, koma sanandiululira. Koma anayamata
a mfumu sanafuna kutambalitsa manja ao kupha ansembe a
Yehova. 18Pamenepo mfumu inati kwa Doegi, Potoloka iwe
nuwaphe ansembewo. Ndipo Doegi wa ku Edomu anapotoloka,
nagwera ansembewo, napha tsikulo makumi asanu ndi atatu
mphambu asanu akubvala efodi wabafuta. 19Ndipo anakantha Nobi
ndiwo mudzi wa ansembe ndi lupanga lakuthwa, anthu amuna ndi
akazi, ana ndi makanda, ng'ombe ndi aburu, ndi nkhosa, ndi
lupanga lakuthwa.

Apulumuka Abyatara

20Ndipo mmodzi wa ana a Ahimeleki, mwana wa Ahitubu, dzina
lace ndiye Abyatara, anapulumuka, nathawira kwa Davide. 21Ndipo
Abyatara anadziwitsa Davide kuti Sauli anapha ansembe a
Yehova. 22Ndipo Davide anati kwa Abyatara, Tsiku lija Doegi wa ku
Edomu anali kumeneko, ndinadziwiratu kuti adzauzadi Sauli; ine
ndinafetsa anthu onse a nyumba ya atate wako. 23Ukhale ndi ine,
usaopa; popeza iye wakufuna moyo wanga afuna moyo wako;
koma ndi ine udzakhala mosungika.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Davide alanditsa a ku Keila

1Tsono anauza Davide, kuti, Onani Afilisti alikuponyana ndi Keila,
nafunkha za m'madwale. 2Cifukwa cace Davide anafunsira kwa
Yehova, nati, Ndimuke kodi kukakantha Afilisti aja? Ndipo Yehova
anati kwa Davide, Muka, nukanthe Afilisti, ndi kupulumutsa
Keila. 3Ndipo anyamata a Davide ananena naye, Taonani, ife
tikhalira m'mantha ku Yuda kuno; koposa kotani nanga tikafika ku
Keila kuponyana ndi makamu a nkhondo a Afilisti. 4Tsono Davide
anafunsiranso kwa Yehova. Ndipo Yehova anamyankha iye, nati,
Nyamuka, nutsikire ku Keila; pakuti ndidzapereka Afilisti m'dzanja
lako. 5Comweco Davide ndi anthu ace anamuka ku Keila,
naponyana ndi Afilisti, natenga ng'ombe zao, nawapha ndi
kuwapulula kwambiri Motero Davide analanditsa okhala m'Keila.
6Ndipo kunali kuti Abyatara mwana wa Ahimeleki pakuthawira kwa
Davide ku Keila, anatsika ali ndi efodi m'dzanja lace. 7Ndipo anthu
anauza Sauli kuti Davide wafika ku Keila. Ndipo Sauli anati,
Mulungu wampereka m'dzanja langa; pakuti atsekerezeka, popeza
analowa m'mudzi wa zitseko ndi mipiringidzo. 8Ndipo Sauli
anamemeza anthu onse kunkhondo, kuti atsikire ku Keila,
kumangira misasa Davide ndi anthu ace. 9Ndipo Davide anadziwa
kuti Sauli analikulingalira zomcitira zoipa; nati kwa Abyatara
wansembe, Bwera kuno ndi efodi. 10Nati Davide, Yehova, Mulungu
wa Israyeli, mnyamata wanu wamva zoona kuti Sauli afuna kudza
ku Keila, kuononga mudziwo cifukwa ca ine. 11Kodi amuna a ku
Keila adzandipereka m'dzanja lace? Kodi Sauli adzatsikira ndithu,
monga mnyamata wanu wamva? Yehova Mulungu wa Israyeli,
ndikupemphani, muuze mnyamata wanu. Ndipo Yehova anati,
Adzatsika. 12Tsono Davide anati, Kodi amuna a ku Keila
adzandipereka ine ndi anyamata anga m'dzanja la Sauli? Ndipo
Yehova anati, Adzakupereka. 13Potero Davide ndi anyamata ace,
ndiwo monga ngati mazana asanu ndi limodzi, ananyamuka,
naturuka ku Keila, nayendayenda kuli konse adakhoza kuyendako.
Ndipo anauza Sauli kuti Davide wapulumuka ku Keila; iye naleka
kumtsata.

Davide ndi Jonatani abwereza kupangana

14Ndipo Davide anakhala m'cipululu m'ngaka, nakhala m'dziko la
mapiri m'cipululu ca Zifi. Ndipo Sauli anamfunafuna masiku onse,
koma Mulungu sadampereka m'dzanja lace. 15Ndipo Davide
anaona kuti Sauli adaturuka kudzafuna moyo wace; Davide
nakhala m'cipululu ca Ziti m'nkhalango. 16Ndipo Jonatani mwana
wa Sauli ananyamuka, napita kwa Davide kunkhalangoko,
namlimbitsa dzanja lace mwa Mulungu. 17Ndipo iye ananena naye,
Usaopa; cifukwa dzanja la Sauli atate wanga silidzakupeza; iwe

udzakhala mfumu ya Israyeli, ndipo ine ndidzakhala wotsatana nawe, icinso Sauli atate wanga acidziwa. 18Ndipo awiriwo anapangana pangano pamaso pa Yehova; ndipo Davide anakhala kunkhalango, koma Jonatani anapita ku nyumba yace. 19Ndipo a ku Zifi anakwera kwa Sauli ku Gibeya, nati, Davide salikubisala kwathu kodi, m'ngaka za m'nkhalango, m'phiri la Hakila. Umene Uri kumwera kwa cipululu? 20Cifukwa cace mfumu, tsikani, monga umo mukhumbire m'mtima mwanu kutsika; ndipo kudzakhala kwathu kumpereka iye m'dzanja la mfumu. 21Sauli nati, Mudalitsike inu kwa Yehova; cifukwa munandicitira ine cifundo. 22Mukanitu kuti mukadziwitse ndithu, ndi kudziwa ndi kuona mbuto m'mene akhalitsa, ndi amene adamuona m'menemo; cifukwa anandiuza kuti iye acita mocenjera ndithu. 23Cifukwa cace yang'anirani, ndi kudziwa ngaka zonse alikubisalamo iye, nimubwere kwa ine ndi mau otsimikizika, pomwepo ndidzamuka nanu; ndipo akakhala m'dzikomo, ndidzampwaira pakati pa mabanja onse a Yuda. 24Ndipo iwo ananyamuka, namuka ku Zifi asanapiteko Sauli; koma Davide ndi anthu ace anali ku cipululu ca Maoni, m'cigwa ca kumwera kwa cipululu. 25Ndipo Sauli ndi anthu ace anamuka kukamfuna. Koma wina anauza Davide; cifukwa cace anatsikira kuthanthweko, nakhala m'cipululu ca Maoni. Ndipo pamene Sauli anamva ici, iye anamlondola Davide m'cipululu ca Maoni. 26Ndipo Sauli anamuka mbali yina ya phiri, Davide ndi anthu ace kutseri kwace; ndipo Davide anafulumira kuthawa, cifukwa ca kuopa Sauli; popeza Sauli ndi anthu ace anazinga Davide ndi anthu ace kwete kuti awagwire. 27Koma mthenga unafika kwa Sauli ndi kuti, Mufulumire kubwerera; popeza nkhondo yobvumbulukira ya Afilisti yalowa m'dziko. 28Comweco Sauli anabwerera polondola Davide, nakakomana ndi Afilisti; cifukwa cace anachula dzina lace la malo aja, Thanthwe lolekanitsa. 29Ndipo Davide anakwera kucokera kumeneko, nakhalam'ngaka za Engedi.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Davide aleka Sauli osamupha

1Ndipo kunali, pakubwerera Sauli potsata Afilisti, anamuuza, kuti, Taonani, Davide ali ku cipululu ca Engedi. 2Tsono Sauli anatenga anthu zikwi zitatu osankhika pakati pa Aisrayeli onse, namuka kukafuna Davide ndi anthu ace m'matanthwe a zinkhoma. 3Ndipo panjira anafika ku makola a nkhosa, kumene kunali phanga; ndipo Sauli analowa kuti akapfunde mapazi ace. Ndipo Davide ndi anyamata ace analikukhala m'kati mwa phangamo, 4Ndipo anyamata a Davide ananena naye, Onani, lero ndilo tsiku limene Yehova anati kwa inu, Onani, Ine ndidzapereka mdani wako m'dzanja lako, kuti ukamcitira iye cokukomera. Ndipo Davide ananyamuka, nadula mkawo wa mwinjiro wa Sauli mobisika. 5Ndipo kunali m'tsogolo mwace kuti a mtima wa Davide unamtsutsa cifukwa adadula mkawo wa mwinjiro wa Sauli. 6Nati kwa anyamata ace, Mulungu andiletse kucitira ici mbuye wanga, wodzozedwa wa Yehova, kumsamulira dzanja langa, popeza iye ndiye wodzozedwa wa Yehova. 7Comweco Davide analetsa anyamata ace ndi mau awa, osawaloleza kuukira Sauli. Ndipo Sauli ananyamuka, naturuka m'phangamo, namuka njira yace. 8Bwino lace Davide yemwe ananyamuka, naturuka m'phangamo, napfuulira Sauli, nati, Mbuye wanga, mfumu. Ndipo pakuceuka Sauli, Davide anaweramira nkhope yace pansi, namgwadira. 9Davide nanena ndi Sauli, Bwanji mulikusamalira mau a anthu akuti, Onani, Davide afuna kukucitirani coipa. 10Onani, lero lomwe maso anu anapenya kuti Yehova anakuperekani inu lero m'dzanja langa m'phangamo, ndipo ena anandiuza ndikupheni; koma ndinakulekani, ndi kuti, Sindidzatukulira mbuye wanga dzanja langa; cifukwa iye ndiye wodzozedwa wa Yehova. 11Ndiponso atate wanga, penyani, inde penyani mkawo wa mwinjiro wanu m'dzanja langa; popeza ndinadula mkawo wa mwinjiro wanu, osakuphani, mudziwe, nimuone kuti mulibe coipa kapena kulakwa m'dzanja langa, ndipo sindinakucimwirani, cinkana inu musaka moyo wanga kuti muugwire, 12Yehova aweruze pakati pa ine ndi inu; ndipo Yehova adzandibwezera cilango kwa inu; koma dzanja langa silidzakhala pa inu. 13Monga umanena mwambi wa makolo, kuti, Ucimo uturukira mwa ocimwa; koma dzanja langa silidzakhala pa inu. 14Nanga mfumu ya Israyeli inaturukira yani; inu mulikupitikitsa yani? Garu wakufa, kapena nsabwe. 15Cifukwa cace Yehova akhale woweruza, naweruze pakati pa ine ndi inu, nayang'anire, oandigwirire moyo, oandipulumutse m'dzanja lanu. 16Ndipo kunali, pakutsiriza Davide kulankhula mau awa kwa Sauli, Sauli anati, Ndiwo mau ako kodi, mwana wanga Davide? Sauli nakweza mau

ace, nalira misozi. 17Nati kwa Davide, Iwe ndiwe wolungama
woposa ine; popeza unandibwezera zabwino, koma ine
ndinakubwezera zoipa. 18Ndipo unatsimikiza lero lino kuti
wandicitira zabwino cifukwa sunandipha pamene Yehova
anandipereka m'dzanja lako. 19Pakuti munthu akapeza mdani
wace, adzamleka kodi kuti acoke bwino? Cifukwa cace Yehova
akubwezere zabwino pa ici unandicitira ine lero lomwe. 20Ndipo
tsono taona ndidziwa kuti udzakhala mfumu ndithu, ndi kuti ufumu
wa Israyeli udzakhazikika m'dzanja lako. 21Cifukwa cace tsono
undilumbirire ndi Yehova, kuti sudzatha mbeu yanga nditamuka
ine, ndi kuti sudzaononga dzina langa m'nyumba ya atate
wanga. 22Ndipo Davide analumbirira Sauli. Sauli namuka kwao;
koma Davide ndi anthu ace anakwera kumka kungaka.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Amwalira Samueli

1Ndipo Samueli anamwalira; ndi Aisrayeli onse anaunjikana
pamodzi nalira maliro ace, namuika m'nyumba yace ku Rama.
Davide nanyamuka, natsikira ku cipululu ca Parana.

Za Davide, Nabala ndi Abigayeli

2Ndipo panali munthu ku Maoni, amene katundu wace anali ku
Karimeli; iyeyu anali womveka ndithu, anali nazo nkhosa zikwi
zitatu, ndi mbuzi cikwi cimodzi; ndipo analikusenga nkhosa zace ku
Karimeli. 3Tsono dzina la munthuyo ndiye Nabala, ndi dzina la
mkazi wace ndiye Abigayeli; ndiye mkazi wa nzeru yabwino, ndi wa
nkhope yokongola; koma mwamunayo anali waphunzo ndi woipa
macitidwe ace; ndipo iye anali wa banja la Kalebi. 4Ndipo Davide
anamva kucipululu kuti Nabala alinkusenga nkhosa zace. 5Davide
natuma anyamata khumi, nanena kwa anyamatawo, Mukwere ku
Karimeli, mumuke kwa Nabala ndi kundilankhulira iye; 6ndipo
muzitero kwa wodalayo, Mtendere ukhale pa inu, mtendere
ukhalenso pa nyumba yanu, ndi mtendere ukhale pa zonse muli
nazo. 7Ndipo tsono ndamva kuti muli nao osenga nkhosa; abusa
anu amene anali ndi ife, sitinawacititsa manyazi, ndipo panalibe
kanthu kao kadasowa, nthawi yonse anakhala iwo ku
Karimeli. 8Mufunse anyamata anu, adzakuuzani; cifukwa cace
muwakomere mtima anyamata awa, pakuti tirikufika tsiku labwino;
mupatse ciri conse muli naco m'dzanja lanu, kwa anyamata anu,
ndi kwa mwana wanu Davide. 9Ndipo pakufika anyamata a Davide,
analankhula ndi Nabala monga mau aja onse m'dzina la Davide,
naleka. 10Koma Nabala anayankha anyamata a Davide nati, Davide
ndani? ndi mwana walese ndani? Makono ano pali anyamata
ambiri akungotaya ambuye ao. 11Kodi ndidzatenga mkate wanga,
ndi madzi anga, ndi nyama imene ndinaphera osenga nkhosa
anga, ndi kuzipatsa anthu amene sindidziwa kumene
afumira? 12Comweco anyamata a Davide anatembenukira ku njira
yao, nabwerera, nadza namuuza monga mwa mau onse
awa. 13Ndipo Davide anati kwa anthu ace, Munthu yense wa inu
amangirire lupanga lace. Namangirira munthu yense lupanga lace;
ndi Davide yemwe anamangirira lupanga lace; ndipo anakwera
kumtsata Davide monga anthu mazana anai, koma mazana awiri
anadika akatundu. 14Koma mnyamata wina anauza Abigayeli,
mkazi wa Nabala, kuti, Onani, Davide anatumiza mithenga
akucokera kucipululu kulankhula mbuye wathu; koma iye
anawakalipira. 15Koma anthu aja anaticitira zabwino ndithu,
sanaticititsa manyazi, ndi panalibe kanthu kadatisowa, nthawi
zonse tinali kuyenderana nao kubusa kuja; 16iwo anatikhalira ngati
linga usana ndi usiku, nthawi yonse tinali nao ndi kusunga

nkhosazo. 17Cifukwa cace tsono mudziwe ndi kulingalira cimene
mudzacita; popeza anatsimikiza mtima kucitira coipa mbuye
wathu, ndi nyumba yace yonse; popeza iye ali woipa, ndipo
munthu sakhoza kulankhula naye. 18Pomwepo Abigayeli
anafulumira, natenga mikate mazana awiri, ndi zikopa ziwiri za
vinyo, nkhosa zisanu zoocaoca, ndi miyeso isanu ya tirigu
wokazinga, ndi ncinci za mphesa zouma zana limodzi, ndi ncinci za
nkhuyu mazana awiri, naziika pa aburu. 19Nati kwa anyamataace,
Nditsogolereni; onani ndidza m'mbuvo mwanu. Koma sanauza
mwamuna wace Nabala. 20Ndipo kudatero pakuberekeka iye pa
buru wace, natsikira pa malo obisika a m'phirilo, onani, Davide ndi
anthu ace analikutsikira kwa iye; iye nakomana nao. 21Koma
Davide adanena, Zoonadi ndasunga cabe zace zonse za kaja kanali
nazo m'cipululu, sikadasowa kanthu ka zace zonse; ndipo iye
anandibwezera zoipa m'malo mwa zabwino. 22Mulungu alange
adani a Davide, ndi kuonjezerapo, ngati ndisiyapo kufikira kuunika
kwa m'mawa, kanthu konse ka iye, kangakhale kamwana
kamphongo. 23Ndipo Abigayeli pakuona Davide, anafulumira
kutsika pa bum, nagwa pamaso pa Davide nkhope yace pansi,
namgwadira, 24Ndipo atagwadira pa mapazi ace anati, Pa ine,
mbuye wanga, pa ine pakhale ucimowo; ndipo mulole mdzakazi
wanu alankhule m'makutu anu, nimumvere mau a mdzakazi
wanu. 25Mbuye wanga, musasamalire munthu uyu woipa, ndiye
Nabala; cifukwa monga dzina lace momwemo iye; dzina lace ndiye
Nabala, ndipo ali nako kupusa; koma ine mdzakazi wanu
sindinaona anyamata a mbuye wanga, amene
munawatumiza. 26Cifukwa cace tsono, mbuye wanga, pali Yehova,
ndipo pali moyo wanu, popeza Yehova anakuletsani kuti
mungakhetse mwazi, ndi kudzibwezera cilango ndi dzanja la inu
nokha, cifukwa cace adani anu, ndi iwo akufuna kucitira mbuye
wanga coipa, akhale ngati Nabala. 27Ndipo mphatso iyi mdzakazi
wanu ndatengera mbuye wanga, ipatsidwe kwa anyamata
akutsata mbuye wanga. 28Mukhululukire kulakwa kwa mdzakazi
wanu; pakuti Yehova adzapatsadi mbuye wanga banja lokhazikika,
pakuti mbuyanga amaponya nkhondo za Yehova; ndipo mwa inu
simudzapezeka coipa masiku anu onse. 29Ngakhale anauka anthu
kukulondolani, ndi kufuna moyo wanu, koma moyo wa mbuye
wanga udzamangika m'phukusi la amoyo lakukhala ndi Yehova
Mulungu wanu; koma iye adzaponya miyoyo ya adani anu
kuwataya monga coturuka m'coponyera mwala. 30Ndipo kudzali,
pamene Yehova anacitira mbuye wanga monga mwa zabwino
zonse adalankhula za inu, ndipo adadzaika inu mukhale kalonga
wa Israyeli; 31mudzakhala opanda cakudodoma naco, kapena
cakusauka naco mtima wa mbuye wanga, cakuti munakhetsa

mwazi wopanda cifukwa, kapena kuti mbuye wanga anabwezera cilango; ndipo Yehova akadzacitira mbuye wanga zabwino, pamenepo mukumbukile mdzakazi wanu. 32Ndipa Davide anati kwa Abigayeli, Alemekezedwe Yehova Mulungu wa Israyeli, amene anakutumiza lero kudzandicingamira ine; 33ndipo, kudalitsike kucenjera kwako, nudalitsike iwe, pakuti unandiletsa kusakhetsa mwazi, ndi kusabwezera cilango ndi dzanja la ine ndekha. 34Pakuti ndithu, Pali Yehova Mulungu wa Israyeli, amene anandiletsa lero kusapweteka iwe, ukadapanda kufulumira kubwera kundicingamira, zoonadi sindikadasiyira Nabala kufikira kutaca kanthu konse, ngakhale mwana wamwamunammodzi. 35Comweco Davide analandira m'dzanja lace zimene iye anamtengera; nanena naye, Ukwere kwanu mumtendere; ona, ndamvera mau ako, ndabvomereza nkhope yako. 36Ndipo Abigayeli anafika kwa Nabala; ndipo, onani, anali ndi madyerero m'nyumba mwace, monga madyerero a mfumu; ndi mtima wa Nabala unasekera kwambiri m'kati mwace, pakuti analedzera kwambiri; m'mwemo uyo sadamuuza kanthu konse, kufikira kutaca. 37Tsono m'mawa vinyo atamcokera Nabala, mkazi wace anamuuza zimenezi; ndipo mtima wace unamyuka m'kati mwace, iye nasanduka ngati mwala. 38Ndipo kunali, atapita masiku khumi, Yehova anamkantha Nabala, nafa. 39Ndipo pamene Davide anamva kuti Nabala adamwalira, iye anati, Alemekezedwe Yehova, amene anaweruza mrandu wa mtonzo wanga wocokera ku dzanja la Nabala, naletsa mnyamata wace pa coipa; ndipo Yehova anabwezera pamutu pa Nabala coipa cace. Ndipo Davide anatumiza wokamfunsira Abigayeli, zakuti amtengere akhale mkazi wace. 40Ndipo anyamata a Davide pakufika kwa Abigayeli ku Karimeli, analankhula naye, nati, Davide anatitumiza kwa inu, kukutengani, mukhale mkazi wace. 41Ndipo iye ananyamuka, nawerama nkhope yace pansi, nati, Onani, mdzakazi wanu ali kapolo wakusambitsa mapazi a anyamata a mbuye wanga. 42Ndipo Abigayeli anafulumira nanyamuka, nakwera pa bum, pamodzi ndi anamwali ace asanu akumtsata; natsatira mithenga ya Davide, nakhala mkazi wace. 43Davide anatenganso Ahinoamu wa ku Yezreeli, ndipo onse awiri anakhala akazi ace. 44Pakuti Sauli anapatsa Mikala, mwana wace, mkazi wa Davide, kwa Paliti mwana wa Loisi, wa ku Galimu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Davide alekanso Sauli osamupha

1Ndipo Azifi anafika kwa Sauli ku Gibeya, nati, Kodi Davide sali
kubisala m'phiri la Hagila, kupenya kucipululu! 2Ndipo Sauli
ananyamuka, natsikira ku cipululu ca Zifi, ndi anthu zikwi zitatu a
Israyeli osankhika, kukafuna Davide m'cipululu ca Zifi. 3Sauli
namanga zithando m'phiri la Hagila kupenya kucipululu kunjira,
Koma Davide anakhala kucipululu, naona kuti Sauli alikumfuna
kucipululu komweko. 4Cifukwa cace Davide anatumiza ozonda,
nazindikira kuti Sauli anabwera ndithu, 5Ndipo Davide ananyamuka
nafika pamalo pala Sauli anamangapo; ndipo Davide adaona
pogona Sauli, ndi Abineri mwana wa Neri kazembe wa khamu lace;
ndipo Sauli anagona pakati pa linga la magareta, ndipo anthu
adamanga zithando pomzinga pace. 6Pamenepo Davide
anayankha nati kwa Ahimeleki Mhiti, ndi Abisai mwana wa Zeruya,
mbale wace wa Yoabu, nati, Adzatsikira nane ndani kumisasako
kwa Sauli? Nati Abisai, Nditsika nanu ndine. 7Comweco Davide ndi
Abisai anafika kwa anthuwo usiku; ndipo onani, Sauli anagona tulo
m'kati mwa linga la magareta, ndi mkondo wace wozika kumutu
kwace; ndi Abineri ndi anthuwo anagona pomzinga iye. 8Ndipo
Abisai anati kwa Davide, Lero Mulungu wapereka mdani wanu
m'dzanja lanu; ndiloleni ndimpyoze ndi mkondo, kamodzi kokha,
sindidzampyoza kawiri. 9Koma Davide ananena ndi Abisai,
Usamuononge, ndani adzasamula dzanja lace pa wodzozedwa wa
Mulungu, ndi kukhala wosacimwa? 10Nati Davide, Pali Yehova,
Yehova adzamkantha iye; kapena tsiku la imfa yace lidzafika;
kapena adzatsikira kunkhondo, nadzafako. 11Yehova andiletse ine
kusamula dzanja langa pa wodzozedwa wa Yehova; koma utenge
mkondowo uli kumutu kwace, ndi cikho ca madzi, ndipo tiyeni,
timuke. 12Comweco Davide anatenga mkondowo, ndi cikho ca
madzi ku mutu wa Sauli nacoka iwowa, osawaona munthu, kapena
kuzidziwa, kapena kugalamuka; pakuti onse anati m'tulo; popeza
tulo tatikuru tocokera kwa Yehova tinawagwira onse. 13Ndipo
Davide anaolokera kutsidya, naima patali pamwamba pa phiri;
pakati pao panati danga lalikuru; 14ndipo Davide anaitana
anthuwo, ndi Abineri mwana wa Neri, nati, Suyankha kodi Abineri?
Tsono Abineri anayankha, nati, Ndiwe yani amene uitana
mfumuyo? 15Davide nati kwa Abineri, Si ndiwe mwamuna weni
weni kodi? ndani mwa Aisrayeli afanafana ndi iwe? Unalekeranji
tsono kudikira mbuye wako, mfumuyo? pakuti anafika wina
kudzaononga mfumu, mbuye wako. 16Ici unacicita siciri cabwino.
Pali Yehova, muyenera kufa inu, cifukwa simunadikira mbuye
wanu, wodzozedwa wa Yehova. Ndipo tsono, penyani mkondo wa
mfumu ndi cikho ca madzi zinali kumutu kwace ziri kuti? 17Ndipo

Sauli anazindikira mau ace a Davide, nati, Ndi mau ako awa, mwana wanga Davide? Nati Davide, Ndi mau anga mfumu, mbuye wanga. 18Nati iye, Cifukwa ninji mbuye wanga amalondola mnyamata wace? pakuti ndacitanji? kapena m'dzanja langa muli coipa cotani? 19Cifukwa cace mbuye wanga mfumu amvere mau a kapolo wace. Ngati ndi Yehova anakuutsirani inu kutsutsana ndi ine, alandire copereka; koma ngati ndi ana a anthu, atembereredwe pamaso pa Yehova, pakuti anandipitikitsa lero kuti ndisalandireko colowa ca Yehova, ndi kuti, Muka, utumikire milungu yina. 20Cifukwa cace tsono, mwazi wanga usagwe pansi kutati ndi Yehova; pakuti mfumu ya Israyeli yaturuka kudzafuna nsabwe, monga munthu wosaka nkhwali pamapiri. 21Pamenepo Sauli anati, Ndinacimwa; bwera, mwana wanga Davide; pakuti sindidzakucitiranso coipa, popeza moyo wanga unati wa mtengo wapatali pamaso pako lero; ona, ndinapusa ndi kulakwa kwakukuru. 22Davide nayankha, nati, Tapenyani lmkondo wa mfumu Abwere mnyamata wina kuutenga. 23Ndipo Yehova adzabwezera munthu yense cilungamo cace ndi cikhulupiriko cace, popeza Yehova anakuperekani lero m'dzanja langa, koma sindinalola kutukulira dzanja langa pa wodzozedwa wa Yehova, 24Ndipo onani, monga lero ndinasamalira ndithu moyo wanu, momwemo usamaliridwe ndithu moyo wanga pamaso pa Yehova, ndipo iye andipulumutse ku masautso onse. 25Pomwepo Sauli anati kwa Davide, Udalitsike iwe, mwana wanga Davide; udzacita ndithu camphamvu, nudzapambana. Comweco Davide anamuka, ndipo Sauli anabwera kwao.

©The Bible Society of Malawi, 1992

1Ndipo Davide ananena mumtima mwace, Tsiku tina Sauli
adzandipha; palibe cina condikomera koma kuti ndithawire ku dziko
la Afilisti; ndipo Sauli adzakhala kakasi cifukwa ca ine,
osandifunanso m'malire onse a Israyeli, momwemo ndidzapulumuka
m'dzanja lace. 2Ndipo Davide ananyamuka, naoloka pamodzi ndi
anthu mazana asanu ndi limodzi amene anali naye, nafika kwa Akisi
mwana wa Maoki, mfumu ya ku Gati. 3Ndipo Davide anakhala ndi
Akisi ku Gati, iye ndi anthu ace, munthu yense ndi a pabanja pace,
inde Davide ndi akazi ace awiri, Ahinoamu wa ku Jezreeli, ndi
Abigayeli wa ku Karimeli, mkazi wa Nabala. 4Ndipo anauza Sauli kuti
Davide anathawira ku Gati; ndipo iye sanamfunanso.
5Ndipo Davide anati kwa Akisi, Ngati mwandikomera mtima,
andipatse malo kumudzi kwina kumiraga, kuti ndikakhale
kumeneko; pakuti mnyamata wanu adzakhala bwanji m'mudzi
wacifumu pamodzi ndi inu? 6Ndipo Akisi anampatsa Zikilaga tsiku
lomweli; cifukwa cace Zikilaga ndi wa mafumu a Yuda kufikira lero
lomwe.
7Ndipo kuwerenga kwace kwa masiku Davide anakhala ku dziko la
Afilisti ndiko caka cimodzi ndi miyezi inai. 8Ndipo Davide ndi anthu
ace anakwera, nathira nkhondo yobvumbulukira pa Agesuri, ndi
Agirezi, ndi Aamaleki; pakuti awa ndiwo anthu akale a m'dziko lija,
njira ya ku Suri kufikira ku dziko la Aigupto. 9Ndipo Davide
anapasula dzikolo, sanasunga ndi moyo mwamuna kapena
wamkazi; natenga nkhosa, ndi ng'ombe, ndi aburu, ndi ngamila,
ndi zobvala; nabwera nafika kwa Akisi. 10Ndipo Akisi anati,
Wapooyana nkhondo ndi yani lero? Nati Davide, Ndi a kumwera
kwa Ayuda, ndi a kumwera kwa Ayerameli, ndi a kumwera kwa
Akeni. 11Ndipo Davide sadasunga wamoyo mwamuna kapena
mkazi, kubwera nao ku Gati; popeza adati, Kuti angatiulule, ndi
kuti, Davide anatero, ndi makhalidwe ace ndi otere, masiku onse
akukhala ku dziko la Afilisti. 12Ndipo Akisi anakhulupirira Davide,
nati Anadziipitsa ndithu pakati pa anthu a Israyeli, cifukwa cace iye
adzakhala mnyamata wanga cikhalire.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Sauli afunsira mkazi wobwebweta ku Endori

1Ndipo kunali masiku aja, Afilisti anasonkhanitsa pamodzi makamu
ao onse kunkhondo, kuti akaponyane ndi Aisrayeli. Ndipo Akisi
ananena ndi Davide, Dziwa kuti zoonadi, udzaturuka nane ndi
nkhondo, iwe ndi anthu ako. 2Ndipo Davide anati kwa Akisi, Potero
mudzadziwe cimene mnyamata wanu adzacita. Ndipo Akisi anati
kwa Davide, Cifukwa cace ndidzakuika iwe ukhale wondisungira
moyo wanga masiku onse.
3M'menemo Samueli ndipo atafa, ndipo Aisrayeli onse atalira
maliro ace, namuika m'Rama, m'mudzi mwao. Ndipo Sauli
anacotsa m'dzikomo obwebweta onse, ndi aula onse. 4Ndipo Afilisti
anasonkhana, nadza namanga misasa ku Sunemu; ndipo Sauli
anasonkhanitsa Aisrayeli onse, namanga iwo ku Giliboa. 5Ndipo
pamene Sauli anaona khamu la Afilisti, anaopa, ndi mtima wace
unanjenjemera kwakukuru. 6Ndipo pamene Sauli anafunsira kwa
Yehova, Yehova sanamyankha ngakhale ndi maloto, kapena ndi
Urimu, kapena ndi aneneri. 7Tsono Sauli anati kwa anyamata ace,
Mundifunire mkazi wobwebweta, kuti ndimuke kwa iye ndi
kumfunsira. Ndipo anyamata ace anati kwa iye, Onani ku Endori
kuli mkazi wobwebweta. 8Ndipo Sauli anadzizimbaitsa nabvala
zobvala zina, nanka iye pamodzi ndi anthu ena awiri, nafika kwa
mkaziyo usiku; nati iye, Undilotere ndi mzimu wobwebwetawo,
nundiukitsire ali yense ndidzakuchulira dzina lace. 9Ndipo mkaziyo
ananena naye, Onani, mudziwa cimene anacita Sauli, kuti analikha
m'dzikomo obwebweta onse, ndi aula; cifukwa ninji tsono
mulikuchera moyo wanga msampha, kundifetsa. 10Ndipo Sauli
anamlumbirira kwa Yehova, nati, Pali Yehova, palibe cilango
cidzakugwera cifukwa ca cinthu ici. 11Pomwepo mkaziyo anati,
Ndikuukitsireni yani? Nati iye, Undiukitsire Samueli. 12Ndipo
mkaziyo pakuona Samueli, anapfuula ndi mau akuru; ndi mkaziyo
analankhula ndi Sauli, nati, Munandinyengeranji? popeza inu ndinu
Sauli. 13Ndipo mfumuvo inanena naye, Usaope, kodi ulikuona
ciani? Mkaziyo nanena ndi Sauli, Ndirikuona milungu irikukwera
kuturuka m'kati mwa dziko. 14Ndipo ananena naye, Makhalidwe
ace ndi otani? nati iye, Nkhalamba irikukwera yobvala mwinjiro.
Pamenepo Sauli anazindikira kuti ndi Samueli, naweramitsa
nkhope yace pansi, namgwadira. 15Ndipo Samueli ananena ndi
Sauli, Wandibvutiranji kundikweretsa kuno? Sauli nayankha,
Ndirikusautsika kwambiri, pakuti Afilisti aponyana nkhondo ndi ine,
ndipo Mulungu anandicokera, osandiyankhanso, kapena ndi
aneneri, kapena ndi maloto; cifukwa cace ndakuitanani, kuti
mundidziwitse cimene ndiyenera kucita. 16Ndip'o Samueli ananena
naye, Ndipo undifunsiranji ine, popeza Yehova anakucokera,

nasandulika mdani wako? 17Ndipo Yehova yekha wacita monga
ananena pakamwa panga; ndipo Yehova wang'amba ufumuwo,
kuucotsa m'dzanja lako, ndi kuupatsa mnansi wako, ndiye
Davide. 18Cifukwa sunamvera mau a Yehova, ndi kukwaniritsa
mkwiyo wace woopsa pa Ameleki, cifukwa cace Yehova wakucitira
cinthu ici lero. 19Ndiponso Yehova adzapereka Israyeli pamodzi ndi
iwe m'dzanja la Afilisti; ndipo mawa iwe ndi ana ako mudzakhala
kuli ine; Yehova adzaperekanso khamu la Aisrayeli m'dzanja la
Afilisti. 20Pomwepo Sauli anagwa pansi tantha, naopa kwakukuru,
cifukwa ca mau a Samueli; ndipo analibe mphamvu; pakuti tsiku
lonse ndi usiku wace wonse anakhala osadya kanthu. 21Ndipo
mkaziyo anafika kwa Sauli, naona kuti ali wobvutika kwambiri,
nanena naye, Onani, mdzakazi wanu anamvera mau anu, ndipo
ndinataya moyo wanga, ndi kumvera mau anu munalankhula ndi
ine. 22Cifukwa cace tsono, mumverenso mau a mdzakazi wanu,
nimundilole kuika kakudya pamaso panu; ndipo mudye, kuti
mukhale ndi mphamvu pakumuka. 23Koma iye anakana, nati,
Sindifuna kudya. Koma anyamata ace, pamodzi ndi mkaziyo
anamkangamiza; iyenamvera mau ao. Comweco anauka pansi,
nakhala pakama. 24Ndipo mkaziyo anali ndi mwana wa ng'ombe
wonenepa m'nyumbamo; ndipo anafulumira, namupha, natenga
ufa naukanyanga mkate wopanda cotupitsa; 25nabwera nazo kwa
Sauli ndi kwa anyamata ace; nadya iwowa. Atatero ananyamuka,
nacoka usiku womwewo.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Afilisti abweza Davide kunkhondo

1Tsono Afilisti anasonkhanitsa makamu ao onse ku Afeki; ndipo
Aisrayeli anamanga ku citsime ca m'Jezreeli. 2Ndipo akalonga a
Afilisti ananyamuka ndi mazana ao ndi zikwi zao; ndipo Davide ndi
anthu ace ananyamuka ndi a pambuyo pamodzi ndi Akisi. 3Ndipo
akalonga a Afilisti anati, Ahebri awa acitanji pano? Ndipo Akisi
ananena kwa akalonga a Afilisti, Uyu si Davide uja mnyamata wa
Sauli, mfumu ya Israyeli, amene wakhala nane masiku awa kapena
zaka izi, ndipo sindinapeza kulakwa mwa iye, kuyambira tsiku lija
anaphatikana nane kufikira lero. 4Koma akalonga a Afilisti anapsa
naye mtima; nanena naye akalonga a Afilisti, Bwezani munthuyu,
abwerere kumalo kwace kumene munamuikako, asatsikire nafe
kunkhondo, kuti kunkhondoko angasanduke mdani wathu; pakuti
uyu adzadziyanjanitsa ninji ndi mfumu yace? Si ndi mitu ya anthu
awa? 5Uyu si Davide kodi amene anamthirirana mang'ombe
m'magulu ao, kuti,

Sauli anapha zikwi zace,
Koma Davide zikwi zace zankhani?

6Ndipo Akisi anaitana Davide, nanena naye, Pali Yehova, wakhala
woongoka mtima, ndipo kuturuka kwako ndi kubwera kwako
pamodzi ndi ine m'gulumo kundikomera; pakuti sindinaona coipa
mwa iwe kuyambira tsiku la kufika kwako kufikira lero; koma
akalongawo sakukomera mtima. 7Cifukwa cace, bwerera, numuke
mumtendere, kuti angaipidwe mtima nawe akalonga a
Afilisti. 8Ndipo Davide ananena ndi Akisi, Koma ndinacitanji? Ndipo
munapeza ciani mu mnyamata wanu nthawi yonse ndiri pamaso
panu kufikira lero, kuti sindingapite kukaponyana nkhondo ndi
adani a mbuye wanga mfumu? 9Ndipo Akisi anayankha nanena ndi
Davide, Ndidziwa kuti pamaso panga uli wabwino, ngati mthenga
wa Mulungu; koma akalonga a Afilisti anena, iye asamuke nafe
kunkhondoko. 10Cifukwa cace ulawirire m'mawa pamodzi ndi
anyamata a mbuye wako amene anabwera nawe; ndipo mutauka
m'mawa, mumuke kutaca. 11Comweco Davide analawirira, iye ndi
anthu ace, kuti amuke m'mawa ndi kubwera ku dziko la Afilisti.
Ndipo Afilisti anakwera ku Jezreeli.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Davide alanditsa a ku Zikilaga m'manja mwa Aamaleki

1Ndipo kunali, pakufika Davide ndi anthu ace ku Zikilaga tsiku
lacitatu, Aamaleki adaponya nkhondo yobvumbulukira kumwera,
ndi ku Zikilaga, nathyola Zikilaga nautentha ndi moto; 2nagwira
akazi ndi onse anali m'mwemo, akuru ndi ang'ono; sanapha
mmodzi, koma anawatenga, namuka. 3Ndipo pamene Davide ndi
anthu ace anafika kumudziko, onani, unatenthedwa ndi moto; ndi
akazi ao ndi ana ao amuna ndi akazi anatengedwa ukapolo. 4Ndipo
Davide ndi anthu amene anali naye anakweza mau ao, nalira
misozi, kufikira analibe mphamvu yakuliranso. 5Ndipo akazi awiri a
Davide anatengedwa ukapolo, Ahinoamu wa ku Jezreeli ndi
Abigayeli mkazi wa Nabala wa ku Karimeli. 6Ndipo Davide
anadololoka kwambiri, pakuti anthu ananena za kumponya iye
miyala, pakuti mtima wao wa anthu onse unali ndi cisoni, yense
cifukwa ca ana ace amuna ndi akazi. Koma Davide anadzilimbikitsa
mwa Yehova Mulungu wace.
7Ndipo Davide ananena ndi Abyatara wansembeyo, mwana wa
Ahimeleki, Unditengere kuno efodi. Abyatara nabwera ndi efodi
kwa Davide. 8Ndipo Davide anafunsira kwa Yehova, nati,
Ndikalondola khamulo ndidzalipeza kodi? Ndipo anamyankha kuti,
Lonriola, pakuti zoonadi udzawapeza, ndi kulanditsa
zonse. 9Comweco Davide anamuka, iye ndi anthu mazana asanu
ndi limodzi anali naye, nafika kukamtsinje Besori, pamenepo
anatsala ena. 10Ndipo Davide anawalondola, iye ndi anthu mazana
anai; koma anthu mazana awiri anatsala m'mbuyo, cifukwa
analema, osakhoza kuoloka kamtsinje Besori. 11Ndipo ena anapeza
M-aigupto kuthengo, nabwera naye kwa Davide, nampatsa
cakudya, nadya iye; nampatsanso madzi kumwa; 12nampatsanso
cigamphu ca ncinci ya nkhuyu ndi ncinci ziwiri za mphesa; ndipo
atadya, moyo wace unabweranso mwa iye; pakuti adagona masiku
atatu ndi usiku wao, osadya cakudya, osamwa madzi. 13Pamenepo
Davide ananena naye, Ndiwe wa yani? ufumira kuti? Nati iye, Ndiri
mnyamata wa ku Aigupto, kapolo wa M-amaleki; mbuye wanga
anandisiya, cifukwa ndinayambodwala apita masiku
atatu. 14Tinathira nkhondo kumwera kwa Akereti ndi ku dziko lija la
Ayuda, ndi kumwera kwa Kalebi; ndipo tinatentha mudzi wa
Zikilaga ndi moto. 15Ndipo Davide ananena naye, Kodi
udzanditsogolera kufikira ku khamulo? Nati iye, Mundilumbirire
kwa Mulungu, kuti simudzandipha, kapena kundipereka m'dzanja
la mbuye wanga, ndipo ndidzatsika nanu kuli khamu
limene. 16Ndipo pamene anatsika naye, onani, iwo anabalalika apo
ponse, analinkudya, ndi kumwa, ndi kudyerera, cifukwa ca
cofunkha zambiri anazitenga ku dziko la Afilisti, ndi ku dziko la

Yuda. 17Ndipo Davide anawakantha kuyambira madzulo kufikira
usiku wa mawa wace; ndipo panalibe munthu mmodzi wa iwowa
anapulumuka, koma anyamata mazana anai oberekeka pa
ngamila, nathawa. 18Ndipo Davide analanditsa zonse anazitenga
Aamaleki, napulumutsa akazi ace awiri. 19Ndipo sikanasoweka
kanthu, kakang'ono kapena kakakuru, ana amuna kapena ana
akazi, kapena cuma kapena dna ciri conse ca zija anazitenga
iwowa; Davide anabwera nazo zonse. 20Ndipo Davide anatenga
nkhosa zonse ndi ng'ombe zonse, zimene anazipitikitsa patsogolo
pa zoweta zao zao, nati, Izi ndi zofunkha za Davide. 21Ndipo
Davide anafika kuli anthu mazana awiri amene analema osakhoza
kutsata Davide, amenenso anawakhalitsa kukamtsinje Besori;
ndipo iwowa anaturuka kucingamira Davide, ndi amene anali naye;
ndipo pakuyandikira Davide anawafunsa ngati ali
bwanji. 22Pamenepo anthu oipa onse, ndi opanda pace a iwo
amene anapita ndi Davide anayankha nati, Popeza sadamuka nafe
sitidzawapatsa kanthu ka zofunkha tidazilanditsa, koma kwa
munthu yense mkazi wace ndi ana ace, kuti acoke nao
namuke. 23Davide nati, Simudzatero, abale anga inu, ndi zimene
anatipatsa ife Yehova, amene anatisunga, napereka m'dzanja lathu
khamu lija linadza kumenyana nafe. 24Ndipo ndani
adzabvomerezana nanu mrandu uwu? Pakuti monga gawo lace la
iye wakumuka kunkhondoko, momwemo lidzakhala gawo lace la
iye wakukhala ndi akatundu, adzagawana cimodzimodzi. 25Ndipo
kuyambira tsiku lija kufikira lero lomwe anaika ici, cikhale lemba
ndi ciweruzo pa Aisrayeli.
26Ndipo pamene Davide anafika ku Zikilaga, anatumizako za
zofunkhazo kwa akuru a Yuda, ndiwo abwenzi ace, nati, Siyi
mphatso yanu ya zofunkha za adani a Yehova. 27Anatumiza kwa
iwo a ku Beteli, ndi kwa iwo a ku Ramoti wa kumwela, ndi kwa iwo
a ku Yatiri; 28ndi kwa iwo a ku Aroeri, ndi kwa iwo a ku Sifimoti, ndi
kwa iwo a ku Estimoa; 29ndi kwa iwo a ku Rakala, ndi kwa iwo a
m'midzi ya Ayerameli, ndi kwa iwo a m'midzi ya Akeni; 30ndi kwa
iwo a ku Horima, ndi kwa iwo a ku Korasani, ndi kwa iwo a ku
Ataki; 31ndi kwa iwo a ku Hebroni, ndi kumalo konse kumene
Davide ndi anthu ace adafoyendayenda.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Sauli ndi ana ace atatu aphedwa ndi Afilisti pa Giliboa

1Ndipo Afilisti anaponyana ndi Aisrayeli; Aisrayeli nathawa pamaso
pa Afilisti, nagwa olasidwa m'phiri la Giliboa. 2Ndipo Afilisti
anapitikitsa, osawaleka Sauli ndi ana ace; ndipo Afilisti anapha
Jonatani, ndi Abinadabu, ndi Malikisua, ana a Sauli. 3Ndipo
nkhondoyo inamkulira Sauli kwambiri, oponya mibvi nampeza;
ndipo iye anasautsika kwakukuru cifukwa ca oponya
mibviyo. 4Tsono Sauli ananena ndi wonyamula zida zace, Solola
lupanga lako, undipyoze nalo; kuti osadulidwa awa angabwere ndi
kundipyoza, ndi kundiseka, Koma woo nyamula zida zace anakana;
cifukwa anaopa ndithu. Cifukwa cace Sauli anatenga lupanga lace
naligwera. 5Ndipo pakuona kuti Sauli anafa, wonyamula zida zace
yemwe, anagwera lupanga lace, nafera limodzi ndi iye. 6Comweco
adamwalira pamodzi Sauli ndi ana ace atatu, ndi wonyamula zida
zace, ndi anthu ace onse, tsiku lomwe lija. 7Ndipo pamene
Aisrayeli akukhala tsidya lina la cigwa, ndi iwo akukhala tsidya la
Yordano, anaona kuti Aisrayeli alikuthawa, ndi kuti Sauli ndi ana
ace anafa, iwowa anasiya midzi yao, nathawa; ndipo Afilisti anadza
nakhala m'menemo. 8Ndipo kunali m'mawa mwace, pakubwera
Afilisti kubvula akufawo, anapeza Sauli ndi ana ace atatu ali akufa
m'phiri la Giliboa. 9Ndipo anadula mutu wace, natenga zida zace,
natumiza m'dziko lonse la Afilisti mithenga yolalikira ku nyumba ya
milungu yao, ndi kwa anthu. 10Ndipo anaika zida zace m'nyumba
ya Asitarote; napacika mtembo wace ku linga la ku
Betisani. 11Koma pamene a ku Jabezi Gileadi anamva zimene
Afilisti anamcitira Sauli, 12ngwazi zonse zinanyamuka ndi kucezera
usiku kuyenda, natenga mtembo wa Sauli, ndi mitembo ya ana
ace, pa linga la Betisani; nafika ku Jabezi Gileadi naitentha
kumeneko. 13Natenga mafupa ao nawaika patsinde pa mtengo uli
m'Jabezi, nasala kudya masiku asanu ndi awiri.

©The Bible Society of Malawi, 1992

2 Samuel

2 Samueli 1

Amuuza Davide za imfa ya Sauli

1NDIPO kunali atamwalira Sauli, pamene Davide anabwera
atawapha Aamaleki, ndipo Davide atakhala ku Zikilaga masiku
awiri; 2pa tsiku lacitatu, onani, munthu anaturuka ku zithando za
Sauli, ali ndi zobvala zace zong'ambika, ndi dothi pamutu pace;
ndipo kunatero kuti iye, pofika kwa Davide, anagwa pansi
namgwadira. 3Ndipo Davide ananena naye, Ufumira kuti iwe? iye
nanena naye, Ndapulumuka ku zithando za Israyeti. 4Ndipo Davide
ananena naye, Kunaonekanji? undiuze. Nayankha iye, Anthu
anathawa kunkhondo, ndipo ambiri anagwa nafa; ndipo Sauli ndi
Jonatani mwana wace anafanso. 5Ndipo Davide ananena ndi
mnyamata wakumuuza, Udziwa bwang kuti Sauli ndi Jonatani
mwana wace anafa? 6Mnyamata wakumuuzayo nati, Pamene
ndinangoyenda pa phiri la Giliboa, ndinaona, Sauli alikuyedzamira
nthungo yace, ndi magareta ndi apakavalo anamyandikiza. 7Ndipo
iye pakuceukira m'mbuyo mwace anandiona, nanditana. Ndipo
ndinayankha, Ndine. 8Nanena, Ndiwe yani? Ndipo ndinayankha
kuti, Ndine M-amaleki. 9Ndipo anati kwa ine, Uime pa ine
nundiphe, cifukwa kuwawa mtima kwandigwera ine, popeza ndikali
moyobe. 10M'mwemo ndinakhala pambali pace ndi kumtsiriza
cifukwa ndinadziwa kuti sangakhalenso ndi moyo wace, atagwa.
Ndipo ndinatenga korona wa pamutu pace, ndi cigwinjiri ca pa
mkono wace, ndabwera nazo kuno kwa mbuye wanga. 11Pomwepo
Davide anagwira zobvala zace nazing'amba; nateronso anthu onse
okhala naye. 12Nabuma, nalira misozi, nasala kudya kufikira
madzulo, cifukwa ca Sauli ndi mwana wace Jonatani, ndi anthu a
Yehova, ndi banja la Israyeli, cifukwa adagwa ndi lupanga. 13Ndipo
Davide ananena ndi mnyamata wakumuuzayo, Kwanu nkuti?
Nayankha, Ine ndine mwana wa mlendo, M-amaleki. 14Ndipo
Davide ananena naye, Bwanji sunaopa kusamula dzanja lako
kuononga wodzozedwa wa Yehova? 15Davide naitana wina wa
anyamatawo, nati, Sendera numkanthe, Ndipo anamkantha, nafa
iye. 16Koma asanafe, Davide adanena naye, Wadziphetsa ndi
mtima wako; cifukwa pakamwa pako padacita umboni
wakukutsutsa ndi kuti, Ine ndinapha wodzozedwa wa Yehova.

Davide alirira Sauli ndi Jonatani

17Ndipo Davide analirira Sauli ndi Jonatani mwana wace ndi
nyimbo iyi ya maliro; 18nawauza aphunzitse ana Ayuda nyimbo iyi
ya Uta, onani inalembedwa m'buku la Jasari:-

19Ulemerero wako, Israyeli, unaphedwa pa misanje yako.
Ha! adagwa amphamvu

20Usacinene ku Gati,
Usacibukitse m'makwalala a Asikeloni,
Kuti ana akazi a Afilisti angasekere,
Kuti ana akazi a osadulidwawo angapfuule mokondwera.
21Mapiri inu a Giliboa,
Pa inu pasakhale mame kapena mvula, kapena minda yakutengako zopereka.
Pakuti kumeneko zikopa za amphamvu zinatayika koipa,
Cikopa ca Sauli, monga ca wosadzozedwa ndi mafuta.
22Uta wa Jonatani sunabwerera,
Ndipo lupanga la Sauli silinabwecera cabe,
Pa mwazi wa ophedwa, pa mafuta a amphamvuwo.
23Sauli ndi Jonatani anali okoma ndi okondweretsa m'miyoyo yao,
Ndipo m'imfa yao sanasiyana; Anali nalo liwiro loposa ciombankanga,
Anali amphamvu koposa mikango.
24Ana akazi inu a Israyeli, mulirire Sauli,
Amene anakubvekani ndi zofira zokometsetsa,
Amene anaika zokometsetsa zagolidi pa zobvala zanu.
25Ha! amphamvuwo anagwa pakati pa nkhondo!
Jonatani anaphedwa pamisanje pako.
26Ndipsinjika mtima cifukwa ca iwe, mbale wanga Jonatani;
Wandikomera kwambiri;
Cikondi cako, ndinadabwa naco,
Cinaposa cikondi ca anthu akazi.
27Ha! amphamvuwo anagwa,
Ndi zida za nkhondo zinaonengeka,

©The Bible Society of Malawi, 1992

Davide alowa ufumu wa Yuda

1Ndipo zitatha izi Davide anafunsira kwa Yehova nati, Kodi
ndikwere kunka m'mudzi wina wa Yuda? Ndipo Yehova ananena
naye, Kwera. Davide nanena naye, Ndikwere kuti? Ndipo anati, Ku
Hebroni. 2Comweco Davide anakwera kunka kumeneko pamodzi
ndi akazi ace awiri, ndiwo Ahingamu Mjezreeli, ndi Abigayeli mkazi
wa Nabala wa ku Karimeli. 3Ndipo Davide anakwera nao anyamata
ace okhala naye, munthu yense ndi banja lace; iwowa nakhala
m'midzi ya Hebroni. 4Ndipo anthu Ayuda anabwera namdzoza
Davide pomwepo akhale mfumu ya nyumba ya Yuda.
Ndipo wina anauza Davide kuti, Anthu a ku Jabezi Gileadi ndiwo
amene anamuika Sauli. 5Pamenepo Davide anatumiza mithenga
kwa anthu a ku Jabezi Gileadi, nanena nao, Mudalitsike ndi Yehova
inu, popeza munacitira cokoma ici mbuye wanu Sauli, ndi
kumuika. 6Ndipo tsopano Yehova acitire inu cokoma ndi coonadi;
inenso ndidzakubwezerani cokoma ici, popeza munacita
cinthuci. 7Cifukwa cace tsono manja anu alimbike, nimucite
camuna; pakuti Sauli mbuye wanu wafa, ndi a nyumba ya Yuda
anandidzoza ndikhale mfumu yao.

Isibosete alowa ufumu wa Israyeli

8Koma Abineri, mwana wa Neri, kazembe wa khamu la ankhondo a
Sauli anatenga Isiboseti mwana wa Sauli, namuolotsa nanka naye
ku Mahanaimu; 9namlonga ufumu wa pa Gileadi ndi Aasuri ndi
Jezreeli ndi Efraimu ndi Benjamini ndi Aisrayeli onse. 10Ndipo
Isiboseti mwana wa Sauli anali ndi zaka makumi anai pakuyamba
iye kukhala mfumu ya Israyeli, nacita ufumu zaka ziwiri. Koma a
nyumba ya Yuda anatsata Davide. 11Ndipo Davide anali mfumu ya
nyumba ya Yuda ku Hebroni zaka zisanu ndi ziwiri kudza miyezi
isanu ndi umodzi.

Ayuda ndi Aisrayeli alimbana ku Gibeoni

12Ndipo Abineri mwana wa Neri ndi anyamata a Isiboseti mwana
wa Sauli anaturuka ku Mahanaimu kunka ku Gibeoni. 13Ndi Yoabu
mwana wa Zeruya, ndi anyamata a Davide anaturuka nakomana
nao pa thamanda la Gibeoni; nakhala pansi, ena tsidya lino, ndi
ena tsidya lija la thamandalo. 14Ndipo Abineri ananena ndi Yoabu,
Aimirire anyamata nasewere pamaso pathu. Nati Yoabu,
Aimirire. 15Pomwepo iwo anaimirira naoloka owerengedwa, khumi
ndi awiri a kwa Benjamini, ndi Isiboseti mwana wa Sauli, ndi khumi
ndi awiri a anyamata a Davide. 16Ndipo anagwirana munthu yense
kugwira mutu wa mnzace, nagwaza ndi lupanga lace m'nthiti mwa
mnzaceo Comweco anagwa limodzi; cifukwa cace malo aja
anachedwa Dera la Mipeni la ku Gibeoni. 17Ndipo tsikulo nkhondo
inakula ndithu. Ndi Abineri ndi anthu a Israyeli anathawa pamaso

pa anyamata a Davide. 18Ndipo analipo ana atatu a Zeruya, ndiwo Yoabu, Abisai ndi Asaheli. Ndipo Asaheli anali waliwiro ngati nyama ya kuthengo. 19Ndipo Asaheli anapitikitsa Abineri. Ndipo m'kuthamanga kwace sanapambukira kulamanja, kapena kulamanzere, pakutsata Abineri. 20Pomwepo Abineri anaceuka nati, Kodi ndi iwe Asaheli? iye nayankha, Ndine. 21Ndipo Abineri ananena naye, Patuka iwe kulamanja kapena kulamanzere kwako nudzigwirire wina wa anyamatawo, nutenge zida zace. Koma Asaheli anakana kupambuka pakumtsata iye. 22Ndipo Abineri anabwereza kunena kwa Asaheli, Pambuka pakunditsata ine. Ndidzakukanthiranji kukugwetsa pansi? ndikatero ndidzaweramutsanso bwanji nkhope yanga kwa mbale wako Yoabu? 23Koma iye anakana kupambuka; cifukwa cace Abineri anamkantha ndi khali la mkondo m'mimba mwace, ndi khalilo linaturuka kumbuyo kwace. Ndipo anagwako, nafera pomwepo, Ndipo onse akufika kumalo kumene Asaheli anagwa, namwalirapo, anaima pomwepo. 24Koma Yoabu ndi Abisai anampitikitsa Abineri; ndipo dzuwa linawalowera pofika ku citunda ca Ama, cakuno ca Giya, pa njira ya ku cipululu ca Gibeoni. 25Ndipo ana a Benjamini anaunjikana pamodzi kutsata Abinen, nakhala gulu limodzi, naima pamwamba pa citunda. 26Pomwepo Abineri anaitana Yoabu nati, Kodi lupanga lidzaononga cionongere? sudziwa kodi kuti kutha kwace kudzakhala udani ndithu? Tsono udzakhalanso nthawi yanji osauza anthu kubwerera pakutsata abale ao? 27Yoabu nati, Pali Mulungu, iwe ukadapandakunena, anthu akadabalalika m'mawa osatsata yense mbale wace. 28Comweco Yoabu anaomba Gpenga, anthu onse naima, naleka kupitikitsa Aisrayeli, osaponyana naonso. 29Ndipo Abineri ndi anthu ace anacezera usiku wonse kupyola cidikha, naoloka Yordano, napyola Bitroni lonse nafika ku Mahanaimu. 30Ndipo Yoabu anabwerera pakutsata Abineri. Ndipo pamene anasonkhanitsa pamodzi anthu onse anasowa anthu a Davide khumi ndi asanu ndi anai ndi Asaheli. 31Koma anyamata a Davide anakantha anthu a Benjamini ndi a Abineri, namwalira mazana atatu mphambu makumi asanu ndi limodzi. 32Ndipo ananyamula Asaheli namuika m'manda a atate wace ali ku Betelehemu. Ndipo Yoabu ndi anthu ace anacezera kuyenda usiku wonse, ndipo kudawacera ku Hebroni.

©The Bible Society of Malawi, 1992

1Ndipo panali nkhondo nthawi yaitali pakati pa nyumba ya Sauli ndi
nyumba ya Davide. Koma Davide analimba cilimbire, ndi nyumba ya
Sauli inafoka cifokere.

Ana obadwira Davide ku Hebroni

2Ndipo ana a Davide anabadwira ku Hebroni. Mwana woyamba
ndiye Amnoni, wa Ahinoamu wa ku Jezreeli; 3waciwiri Kileabu, wa
Abigayeli mkazi wa Nabala wa ku Karimeli; ndi wacitatu Abisalomu
mwana wa Maaka mwana wamkazi wa Talimai mfumu ya ku
Gesuri; 4ndi wacinai Adoniya mwana wa Hagiti; ndi wacisanu
Sefatiya mwana wa Abitali; 5ndi wacisanu ndi cimodzi Itireamu wa
Egila mkazi wa Davide. Awa anambadwira Davide ku Hebroni.

Abineri apangana ndi Davide

6Ndipo panali, pokhala nkhondo pakati pa nyumba ya Sauli ndi
nyumba ya Davide, Abineri analimbikira nyumba ya Sauli. 7Ndipo
Sauli adali ndi mkazi wamng'ono, dzina lace ndiye Rizipa, mwana
wa Aya. Ndipo Isiboseti anati kwa Abineri, Unalowana bwanji ndi
mkazi wamng'ono wa atate wanga? 8Pomwepo Abineri anapsa
mtima kwambiri pa mau a Isiboseti, nati, Ndine mutu wa gam wa
Yuda kodi? Lero lino ndirikucitira zokoma nyumba ya Sauli atate
wanu, ndi abale ace, ndi abwenzi ace, ndipo sindinakuperekani
m'dzanja la Davide, koma mundinenera lero lino za kulakwa naye
mkazi uyu. 9Mulungu alange Abineri, naonjezepo, ndikapanda
kumcitira Davide monga Yehova anamlumbirira; 10kucotsa ufumu
ku nyumba ya Sauli ndi kukhazika mpando wadfumu wa Davide pa
Israyeli ndi pa Yuda, kuyambira ku Dani kufikira ku
Beereseba. 11Ndipo iye sanakhoza kuyankha Abineri mau amodzi
cifukwa ca kumuopa iye.

12Ndipo Abineri anatuma mithenga imnenere kwa Davide, nati,
Dziko nla yani? natinso, Mupangane nane pangano lanu, ndipo
onani, ndidzagwirizana nanu ndi kukopa Aisrayeli onse atsate
inu. 13Nati iye, Cabwino, ndidzapangana nawe; koma ndikuikira
cinthu cimodzi, ndico kuti, sudzaona nkhope yanga, koma utsogole
wabwera naye Mikala mwana wamkazi wa Sauli, pamene ubwera
kudzaona nkhope yanga. 14Ndipo Davide anatumiza mithenga kwa
Isiboseti mwana wa Sauli, nati, Undipatse mkazi wanga Mikala
amene ndinadzitomera ndi nsonga za makungu za Afilisti zana
limodzi. 15Pomwepo Isiboseti anatumiza namcotsera kwa
mwamuna wace, kwa Palitieli mwana wa Laisi. 16Ndipo mwamuna
waceyo anapita naye, nanka nalira, namtsata kufikira ku
Baburimu. Pomwepo Abineri ananena naye, Coka, bwerera; ndipo
anabwerera.

17Ndipo Abineri analankhula nao akuru a Israyeli nanena nao, Inu
munayamba kale kufuna Davide akhale mfumu yanu; 18citani

tsono, popeza Yehova analankhula za Davide, kuti, a Ndi dzanja la Davide mnyamata wanga ndidzapulumutsa anthu anga Aisrayeli ku dzanja la Afilisti, ndi ku dzanja la adani ao onse. 19Ndipo Abineri analankhulanso m'kumva kwa Abenjamini; Abineri anamukanso ku Hebroni kulankhula m'makutu a Davide zonse zakukomera Aisrayeli ndi a nyumba yonse ya Benjamini. 20Abineri nafika kwa Davide ku Hebroni, ali ndi anthu makumi awiri. Ndipo Davide anawakonzera Abineri ndi anthu okhala naye madyerero. 21Pomwepo Abined anati kwa Davide, Ndidzanyamuka ndi kupita ndi kusonkhanitsira mfumu mbuye wanga Aisrayeli onse, kuti adzapangane nanu pangano, ndi kuti mukhale mfumu pa zonse mtima wanu uzikhumba. Comweco Davide analawirana ndi Abineri, namuka iye mumtendere.

Yoabu apha Abineri

22Ndipo taonani, anyamata a Davide ndi Yoabu anabwera kucokera ku nkhondo yobvumbulukira, nakhala nazo zofunkha zambiri. Koma Abineri sanali ku Hebroni kwa Davide, cifukwa adalawirana naye ndipo adamuka mumtendere. 23Tsono pofika Yoabu ndi khamu lonse anali nalo, ena anamfotokozera Yoabu nati, Abineri mwana wa Neri anabwera kwa mfumu, amene analawirana naye, namuka iye mumtendereo 24Pomwepo Yoabu anadza kwa mfumu, nati, Mwacitanji? Taonani, Abineri anadza kwa inu, cifukwa ninji tsono munalawirana naye kuti acokedi. 25Mumdziwa Abineri mwana wa Neri kuti anadza kuti akunyengeni, ndi kuti adziwe kuturuka kwanu ndi kulowa kwanu, ndi kuti adziwe zonse mulikucita inu. 26Ndipo Yoabu anaturuka kwa Davide, natumizira Abineri mithenga, amene anambweza ku citsime ca Sira. Koma Davide sanacidziwa. 27Pofikanso Abineri ku Hebroni, Yoabu anampambutsa kupita nave pakati pa cipata kulankhula naye poduka mphepo; namgwaza pomwepo m'mimba, nafa, cifukwa ca mwazi wa Asaheli mbale wace. 28Ndipo pambuyo pace, pakucimva Davide, anati, Ine ndi ufumu wanga tikhala osacimwira mwazi wa Abineri mwana wa Neri, nthawi zonse, pamaso pa Yehova; 29cilango cigwere pa mutu wa Yoabu ndi pa nyumba yonse ya atate wace; ndipo kusasoweke ku nyumba ya Yoabu munthu wakukhala nayo nthenda yakukha, kapena wakhate, kapena woyenda ndi ndodo, kapena wakugwa ndi lupanga, kapena wakusowa cakudya. 30Motero Yoabu ndi Abisai mbale wace adapha Abineri, popeza iye adapha mbale wao Asaheli ku Gibeoni, kunkhondo.

Davide alira Abineri

31Ndipo Davide anati kwa Yoabu ndi kwa anthu onse okhala naye, Ng'ambani zobvala zanu, ndi kudzimangira ziguduli m'cuuno, nimulire Abineri. Ndipo mfumu Davide anatsata cithatha. 32Ndipo

anaika Abineri ku Hebroni; ndi mfumu inakweza mau ace nilira ku
manda a Abineri, nalira anthu onse. 33Ndipo mfumu inanenera
Abineri nyimbo iyi ya maliro, niti,
Kodi Abineri anayenera kufa ngati citsiru?
34Manja anu sanamangidwa, mapazi anu sanalongedwa
m'zigologolo;
Monga munthu wakugwa ndi anthu oipa momwemo mudagwa inu.
Ndipo anthu onse anamliranso. 35Ndipo anthu onse anadza
kudzadyetsa Davide cakudya kukali msana; koma Davide
analumbira nati, Mulungu andilange naonjezepo, ngati ndilawa
mkate kapena kanthu kena, lisanalowe dzuwa. 36Ndipo anthu onse
anacisamalira, ndipo cinawakomera; ziri zonse adazicita mfumu
zidakomera anthu onse. 37Momwemo anthu onse ndi Aisrayeli onse
anazindikira tsiku lija kuti sikunafumira kwa mfumu kupha Abineri
mwana wa Neri. 38Ndipo mfumu inati kwa anyamata ace,
Simudziwa kodi kuti kalonga, ndi munthu womveka, wagwa lero
m'Israyeli? 39Ndipo ndikali wofoka ine lero, cinkana ndinadzozedwa
mfumu; ndipo amuna awa ana a Zeruya andikakalira mtima;
Yehova abwezere wocita coipa monga mwa coipa cace.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Isiboseti aphedwa, Davide alanga omupha

1Ndipo pamene Isiboseti mwana wa Sauli, anamva kuti Abineri
adakafera ku Hebroni, manja ace anafoka, ndi Aisrayeli onse
anabvutika. 2Ndipo Isiboseti, mwana wa Sauli anali nao amuna
awiri, ndiwo atsogoleri a magulu; wina dzina lace Baana, ndi dzina
la mnzace ndiye Rekabu, ndiwo ana a Rimoni wa ku Beeroti, wa
ana a Benjamini, pakuti Beeroti womwe unawerengedwa wa
Benjamini; 3ndi Abeeroti anathawira ku Gitaimu; kumeneko
amakhalira kufikira lero lino.
4Ndipo Jonatani mwana wa Sauli, anali ndi mwana wamwamuna
wopunduka mapazi, Iyeyu anali wa zaka zisanu muja inamveka
mbiri ya Sauli ndi Jonatani yocokera ku Jezreeli; ndipo mlezi wace
adamnyamula nathawa; ndipo kunali pofulumira kuthawa, iye
anagwa nakhala wopunduka. Dzina lace ndiye Mefiboseti.
5Ndipo Rekabu ndi Baana ana a Rimoni wa ku Beeroti, anamuka,
nafika ku nyumba ya Isiboseti potentha dzuwa popumula iye
usana. 6Ndipo iwo analowanso kufikira m'kati mwa nyumba,
monga ngati anadzatenga tirigu; namgwaza m'mimba mwace; ndi
Rekabu ndi Baana mbale wace anathawa. 7Koma polowa iwo
m'nyumbamo iye ali cigonere pakama pace m'cipindamo,
anamkantha, namupha namdula mutu wace, nautenga namuka
njira ya kucidikha usiku wonse, 8Ndipo anabwera nao mutu wa
Isiboseti kwa Davide ku Hebroni, nanena ndi mfumu, Taonani mutu
wa Isiboseti mwana wa Sauli, mdani wanu amene anafuna moyo
wanu; Yehova anabwezerera cilango mbuye wanga mfumu lero lino
kwa Sauli ndi mbeu yace. 9Ndipo Davide anayankha Rekabu ndi
Baana mbale wace, ana a Rimoni wa ku Beeroti, nanena nao, Pali
Yehova amene anaombola moyo wanga m'masautso onse, 10muja
munthu wina anandiuza kuti, Onani Sauli wamwalira, ndi
kulingalira kuti alikubwera nao uthenga wabwino, ndinamgwira ndi
kumupha ku Zikilaga, ndiyo mphotho yace ndinampatsa cifukwa ca
uthenga wace. 11Koposa kotani nanga, pamene anthu oipa anapha
munthu wolungama pa kama wace m'nyumba yace yace,
ndidzafunsira mwazi wace ku dzanja lanu tsopano, ndi kukucotsani
ku dziko lapansi? 12Ndipo Davide analamulira anyamata ace, iwo
nawapha, nawapacika m'mbali mwa thamanda ku Hebroni
atawadula manja ndi mapazi ao. Koma mutu wa Isiboseti
anautenga nauika m'manda a Abineri ku Hebroni.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Mafuko onse abvomereza Davide mfumu yao

1Pomwepo mafuko onse a Israyeli anabwera kwa Davide ku
Hebroni, nalankhula nati, Taonani, ife ndife pfupa lanu ndi mnofu
wanu. 2Masiku anapitawo, pamene Sauli anali mfumu yathu, inu
ndinu amene munatsogolera Aisrayeli kuturuka nao ndi kubwera
nao; ndipo Yehova ananena nanu, Uzidyetsa anthu anga Israyeli,
ndi kukhala mtsogoleri wa Israyeli, 3Comweco akuru onse a Israyeli
anadza kwa mfumu ku Hebroni; ndipo mfumu Davide anapangana
nao pangano ku Hebroni pamaso pa Yehova; ndipo anamdzoza
Davide mfumu ya Israyeli.
4Davide anali ndi zaka makumi atatu polowa iye ufumu wace,
nakhala mfumu zaka makumi anai. 5Ku Hebroni anacita ufumu pa
Yuda zaka zisanu ndi ziwiri kudza miyezi isanu ndi umodzi; ndi ku
Yerusalemu anacita ufumu pa Aisrayelionse ndi Ayuda omwe zaka
makumi atatu mphambu zitatu.

Davide alanda Yerusalemu

6Ndipo mfumu ndi anthu ace anamuka ku Yerusalemu kuyambana
nao Ajebusi, nzika za dziko; ndiwo ananena kwa Davide ndi kuti,
Sudzalowa muno, koma akhungu ndi opunduka adzakupitikitsa;
ndiko kunena kuti, Davide sakhoza kulowa muno. 7Cinkana anatero
Davide anathyola linga la Ziyoni, lomwelo ndilo mudzi wa
Davide. 8Ndipo tsiku lija Davide anati, Ali yense akakantha Ajebusi,
aponye m'madzi opuala ndi akhungu amene moyo wa Davide
udana nao. Cifukwa cace akuti, Akhungu ndi opuala sangalowe
m'nyumbamo. 9Ndipo Davide anakhala m'linga mula, nalicha
mudzi wa Davide. Davide namanga linga pozinga ponse kuyambira
ku Milo ndi m'kati momwe. 10Ndipo Davide anakula cikulire cifukwa
Yehova Mulungu wa makamu anali naye.
11Ndipo Hiramu mfumu ya Turo anatumiza mithenga kwa Davide
ndi mitengo yamkungudza, ndi amisiri a matabwa, ndi omanga
nyumba; iwo nammangira Davide nyumba. 12Ndipo Davide
anazindikira kuti Yehova anamkhazikitsa mfumu ya Israyeli, ndi
kuti anakulitsa ufumu wace cifukwa ca anthu ace Israyeli.
13Ndipo Davide anadzitengera akazi ang'ono ena ndi akazi a ulemu
ena a ku Yerusalemu, atafikako kucokera ku Hebroni; ndipo
anambadwira Davide ana amuna ndi akazi. 14Maina a iwo
anambadwira m'Yerusalemu ndi awa: Samua, ndi Sobabu, ndi
Natani, ndi Solomo, 15ndi Ibara ndi Elisua, ndi Nefegi ndi
Yafiya; 16ndi Elisama ndi Eliada ndi Elifeleti.

Davide akantha Afilisti

17Koma pamene Afilisti anamva kuti adamdzoza Davide mfumu ya
Israyeli, Afilisti onse anakwera kukafuna Davide; ndipo Davide
anacimva natsikira kungaka kuja. 18Tsono Afilisti anafika natanda

m'cigwa ca Refaimu. 19Ndipo Davide anafunsira kwa Yehova nati,
Kodi ndimuke kuyambana nao Afilistiwo? Mudzawapereka m'dzanja
langa kodi? Ndipo Yehova ananena ndi Davide, Pita, pakuti zoonadi
ndidzapereka Afilisti m'dzanja lako. 20Ndipo Davide anafika ku
Baalaperazimu, nawakantha kumeneko Davideyo; nati, Yehova
wathyola adani anga pamaso panga ngati madzi okamulira.
Cifukwa cace analicha dzina la malowo Baalaperazimu. 21Ndipo
iwo anasiya kumeneko mafano ao; Davide ndi anyamata ace
nawacotsa.
22Ndipo Afilisti anakweranso kaciwiri, natanda m'cigwa ca
Refaimu. 23Ndipo pamene Davide anafunsira kwa Yehova, iye
anati, Usamuke, koma ukawazungulire kumbuyo kuti
ukawaturukire pandunji pa mkandankhuku. 24Ndipo kudzali,
pakumva iwe kuwayula ku nsonga za mkandankhuku, pomwepo
fulumiratu, pakuti pamenepo Yehova waturuka pamaso pako
kukakantha khamu la Afilisti. 25Ndipo Davide anatero, monga
Yehova anamlamulira, nakantha Afilisti kuyambira ku Geba kufikira
ku Gezeri.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Atenga likasa la Mulungu ku nyumba ya Abinadabu

1Pambuyo pace Davide anamemezanso osankhika onse a
m'Israyeli, anthu zikwi makumiatatu. 2Ndipo Davide ananyamuka,
namuka nao anthu onse anali naye, nacokera ku Baale-Yuda
natengako likasa la Mulungu, limene amachula nalo Dzinalo Dzina
la Yehova wa makamu, wokhala pakati pa Akerubi. 3Ndipo iwo
ananyamulira likasa la Mulungu pa gareta watsopano, ataliturutsa
m'nyumba ya Abinadabu, iri pacitunda, ndipo Uza ndi Ahio ana a
Abinadabu anayendetsa ng'ombe za pa gareta
watsopanoyo. 4Poturuka nalo tsono pamodzi ndi likasa la Mulungu
m'nyumba ya Abinadabu iri pacitunda, Ahio anatsogolera
likasalo. 5Ndipo Davide ndi a nyumba yonse ya Israyeli anasewera
pamaso pa Yehova, ndi zoyimbira za mitundu mitundu za
mlombwa, ndi azeze, ndi zisakasa ndi malingaka, ndi masece, ndi
nsanje. 6Ndipo pofika iwo ku dwale la Nakoni, Uza anatambasula
dzanja lace, nacirikiza likasa la Mulungu; cifukwa ng'ombe
zikadapulumuka. 7Pomwepo mkwiyo wa Yehova udayaka pa Uza,
ndipo Mulungu anamkantha pomwepo, cifukwa ca kusalingiriraku;
nafa iye pomwepo pa likasa la Mulungu. 8Ndipo kudaipira Davide,
cifukwa Yehova anacita cipasulo ndi Uza; nacha-malowo Cipasulo
ca Uza, kufikira lero lino. 9Ndipo Davide anaopa Yehova tsiku
lomwelo; nati, Ngati likasa la Yehova lidzafika kwa
ine? 10Momwemo Davide sanafuna kudzitengera likasa la Yehova
lidze ku mudzi wa Davide; koma Davide analipambutsira ku
nyumba ya Obedi-Edomu Mgiti. 11Ndipo a likasa la Yehova
linakhala m'nyumba ya Obedi-Edomu Mgiti miyezi itatu; ndipo
Yehova anadalitsa Obedi-Edomu ndi banja lace lonse.

Akwera nalo likasalo kuleka ku Yerusalemu

12Pamenepo anthu anauza mfumu Davide, kuti Yehova wadalitsa
banja la Obedi-Edomu ndi zace zonse, cifukwa ca likasa la
Mulungu. Comweco Davide anamuka nakatenga likasa la Mulungu
ku nyumba ya Obedi-Edomu, nakwera nalo ku mudzi wa Davide, ali
ndi cimwemwe. 13Ndipo kunali, pamene akunyamula likasa la
Yehova atayenda mapazi asanu ndi limodzi, iye anapha nsembe
ng'ombe ndi conenepa cina. 14Ndipo Davide anabvina ndi
mphamvu yace yonse pamaso pa Yehova; Davide nadzimangirira
efodi wabafuta. 15Comweco Davide ndi a nyumba yonse ya Israyeli
anakwera nalo likasa la Yehova, ndi cimwemwe ndi kulira kwa
malipenga, 16Ndipo kunali pamene likasa la Yehova tinafika
m'mudzi wa Davide, Mikala mwana wamkazi wa Sauli,
analikupenya pazenera, naona mfumu Davide alikubvina ndi
kusewera pamaso pa Yehova, nampeputsa mumtima
mwace. 17Ndipo pamene adalowa nalo likasa la Mulungu analgka

pamalo pace pakati pa hema amene Davide adaliutsira; ndipo Davide anapereka nsembe zopsereza, ndi nsembe zoyamika pamaso pa Yehova. 18Pamene Davide adatsiriza kupereka nsembe yopsereza ndi zoyamika, iye anawadalitsa anthuwo m'dzina la Yehova wa makamu. 19Ndipo anagawira anthu onse, ndiwo unyinji wonse wa Israyeli, amuna ndi akazi, kwa munthu yense mtanda wa mkate ndi nthuli ya nyama, ndi ncinci ya mphesa, Ndipo anthu aja onse anabwera yense ku nyumba yace. 20Pamenepo Davide anabwerera kudalitsa nyumba yace. Ndipo Mikala mwana wamkazi wa Sauli anaturukira kwa Davide, nati; Ha! Lero mfumu ya Israyeli inalemekezeka ndithu, amene anabvula lero pamaso pa adzakazi a anyamata ace, monga munthu woluluka abvula wopanda manyazi! 21Koma Davide ananena ndi Mikala, Ndatero pamaso pa Yehova, amene anandisankha ine ndi kupitirira atate wako ndi banja lace lonse, nandiika ndikhale mtsogoleri wa anthu a Yehova, wa Israyeli, cifukwa cace ndidzasewera pamaso pa Yehova. 22Ndipo ndidzaonjezanso kukhala ngati munthu woluluka, ndidzakhala wodzicepetsa m'maso a ine mwini; ndipo adzakazi udanenawo, ndi amenewo ndidzalemekezedwa. 23Ndipo Mikala mwana wamkazi wa Sauli sanaona mwana kufikira tsiku la imfa yace.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Mulungu salola Davide ammangire nyumba

1Ndipo kunali pakukhala mfumuyo m'nyumba mwace,
atampumulitsa Yehova pa adani ace onse omzungulira, 2mfumuyo
inanena ndi Natani mneneriyo, Onani ndirikukhala ine m'nyumba
yamikungudza, koma likasa la Mulungu liri m'kati mwa nsaru
zocinga. 3Ndipo Natani anati kwa mfumuyo, Mukani mucite conse
ciri mumtima mwanu, pakuti Yehova ali nanu, 4Ndipo kunali usiku
womwewo mau a Yehova anafika kwa Natani, kuti, 5Kauze mtumiki
wanga Davide, kuti, Atero Yehova, Kodi iwe udzandimangira
nyumba yakuti ndikhalemo Ine? 6pakuti sindinakhala m'nyumba
kuyambira tsiku lija ndinaturutsa ana a Israyeli ku Aigupto kufikira
lero lomwe, kama ndinayenda m'cihema ndi m'nyumba
wamba. 7M'malo monse ndinayendamo limodzi ndi ana onse a
Israyeli kodi ndinanena ndi pfuko limodzi la Aisrayeli, limene
ndinalamulira kudyetsa anthu anga Aisrayeli, kuti, Munalekeranji
kundimangira nyumba yamikungudza? 8Cifukwa cace tsono
udzatero kwa mtumiki wanga Davide, Atero Yehova wa makamu,
Ndinakucotsa kubusako kumene unalikutsata nkhosa kuti
udzakhale mfumu ya anthu anga, ndiwo Israyeli, 9Ndipo ndinali
nawe kuli konse unamukako, ndi kuononga adani ako onse pamaso
pako; ndipo ndidzamveketsa dzina lako, monga dzina la akuru ali
pa dziko lapansi, 10Ndipo ndidzaikira anthu anga Israyeli malo, ndi
kuwaoka kuti akakhale m'malo ao a iwo okha, osasunthikanso.
Ndipo anthu a mphulupulu sadzawabvutanso, monga poyamba
paja, 11monga kuyambira tsiku lija ndinalamulira oweruza
kuyang'anira anthu anga Israyeli; ndipo ndidzakupumulitsa kwa
adani ako onse. Yehova akuuzanso kuti Yehova adzakumangira
banja. 12Pamene masiku ako akadzakwaniridwa, ndipo iwe
udzagona ndi makolo ako, Ine ndidzaukitsa mbeu yako pambuyo
pako, imene idzaturuka m'matumbo mwako, ndipo
ndidzakhazikitsa ufumu wace. 13Iye adzamangira dzina langa
nyumba, ndipo ndidzakhazikitsa cimpando ca ufumu wace ku
nthawi zonse. 14Ndidzakhala atate wace, iye nadzakhala mwana
wanga; akacita coipa ndidzamlanga ndi ndodo ya anthu, ndi
mikwapulo ya ana a anthu; 15koma cifundo canga sicidzamcokera
iye, monga ndinacicotsera Sauli amene ndinamcotsa pamaso
pako. 16Ndipo nyumba yako ndi ufumu wako zidzakhazikikadi ku
nthawi zonse pamaso pako; mpando wacifumu wako udzakhazikika
ku nthawi zonse. 17Monga mwa mau onse awa ndi monga mwa
masomphenya onse awa, momwemo Natani analankhula ndi
Davide.
18Pomwepo Davide mfumu analowa, nakhalapansi pamaso pa
Yehova; nati, Ine ndine yani, Yehova Mulungu, ndi banja langa ndi

ciani kuti munandifikitsa pano? 19Ndipo icinso cinali pamaso panu cinthu cacing'ono, Yehova Mulungu; koma munanenanso za banja la mnyamata wanu kufikira nthawi yaikuru irinkudza; ndipo mwatero monga mwa macitidwe a anthu, Yehova Mulungu! 20Ndipo Davide adzaonjezanso kunenanso ndi Inuj pakuti mudziwa mnyamata wanu, Yehova Mulungu. 21Cifukwa ca mau anu, ndi monga mwa mtima wanu, munacita ukuru wonse umene kuuzindikiritsa mnyamata wanu. 22Cifukwa cace wamkuru ndi Inu Yehova. Mulungu, pakuti palibe wina wofanana ndi Inu, palibe Mulungu winanso koma Inu, monga mwa zonse tinazimva ndi makutu athu. 23Ndiponso mtundu uti wa pa dziko lapansi ufanana ndi anthu anu, ndiwo Israyeli, amene Mulungu anakadziombolera akhale anthu ace, ndi kuti limveke dzina lace, ndi kukucitirani zinthu zazikuru ndi kucitira dziko lanu zoopsa, pamaso pa anthu anu, amene munadziombolera kuwaturutsa ku dziko la Aigupto mwa amitundu ndi milungu yao? 24Ndipo mwadzikhazikira anthu anu Aisrayeli, akhale anthu anu nthawi zonse, ndipo Inu Yehova munakhala Mulungu wao. 25Ndipo tsopano, Yehova Mulungu, mau amene munalankhula za mnyamata wanu ndi za nyumba yace, muwalimbikitse ku nthawi zonse nimucite monga munalankhula. 26Ndipo dzina lanu likulitsidwe ku nthawi zonse, kuti Yehova wit makamu ndiye Mulungu wa Israyeli, ndi nyumba ya mnyamata wanu Davide idzakhazikika pamaso panu. 27Pakuti inu, Yehova wa makamu, Mulungu wa Israyeli, munaulula kwa mnyamata wanu kuti, Ndidzakumangira iwe nyumba; cifukwa cace mnyamata wanu analimbika mtima kupemphera pemphero gi kwa Inu. 28Ndipo tsopano, Yehova Mulungu, Inu ndinu Mulungu, ndi mau anu adzakhala oona, ndipo Inu munaloniezana ndi mnyamata wanu kumcitira cabwino ici, 29cifukwa cace tsono cikukomereni kudalitsa nyumba ya mnyamata wanu kuti ikhale pamaso panu cikhalire; pakuti Inu, Yehova Mulungu, munacinena; ndipo nyumba ya mnyamata wanu idalitsike ndi dalitso lanu ku nthawi zonse.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Davide agonjetsa amitundu ena

1Ndipo m'tsogolo mwace Davide anakantha Afilisti, nawagonjetsa;
Davide nalanda mudzi wa Metege Ama m'manja mwa
Afilisti. 2Ndipo anakantha Amoabu nawayesa ndi cingwe,
nawagonetsa pansi; ndipo anawayesera zingwe ziwiri kupha, ndi
cingwe cimodzi cathunthu kusunga ndi moyo. Ndipo Amoabu
anakhala anthu a Davide, nabwera: nayo mitulo. 3Davide
anakanthanso Hadadezeri, mwana wa Rehobu, mfumu ya ku Zoba,
pomuka iye kukadzitengeranso ufumu wace ku cimtsinje ca
Firate. 4Ndipo Davide anatenga apakavalo ace cikwi cimodzi
mphambu mazana asanu ndi awiri, ndi oyenda pansi zikwi maku
mi awiri; ndipo Davide anadula mitsita akavalo onse a magareta,
koma anasunga a iwo akufikira magareta zana limodzi. 5Ndipo
pakufika Aaramu a ku Damasiko kudzathandiza Hadadezeri mfumu
ya ku Zoba, Davide anakanthako Aaramu zikwi makumi awiri
mphambu ziwiri. 6Pamenepo Davide anaika maboma m'Aramu wa
Damasiko, Ndipo Aaramu anasanduka anthu a Davide, nabwera
nayo mitulo. Ndipo Yehova anamsunga Davide kuli konse
anamukako. 7Ndipo Davide anatenga zikopa zagolidi zinali ndi
anyamata a Hadadezeri, nabwera nazo ku Yerusalemu. 8Ndipo ku
Beta ndi ku Berotai midzi ya Hadadezeri, mfumu Davide anatenga
mikuwa yambiri ndithu. 9Ndipo pamene Toi mfumu ya ku Hamati
anamva kuti Davide adakantha khamu lonse la Hadadezeri, 10Toi
anatumiza mwana wace Joramu kwa mfumu Davide, kuti
akamlankhule iye, ndi kumdalitsa, popeza anamenyana ndi
Hadadezeri ndi kumkantha; pakuti pakati pa Hadadezeri ndi Toi
panali nkhondo. Ndipo Joramu anabwera ndi zotengera zasiliva, ndi
zotengera zagolidi, ndi zotengera zamkuwa. 11Izi zomwe mfumu
Davide anazipatula zikhale za Yehova, pamodzi ndi siliva ndi golidi
anapatulako za amitundu onse adawagonjetsa; 12za Aaramu, za
Amoabu, za ana a Amoni, za Afilisti, za Amaleki, ndi zofunkha za
Hadadezeri, mwana wa Rehobu mfumu ya ku Zoba. 13Ndipo
Davide anamveketsa dzina lace pamene anabwera uko adakantha
Aaramu m'cigwa ca mcere, ndiwo anthu zikwi khumi mphambu
zisanu ndi zitatu. 14Ndipo anaika maboma m'Edomu; m'dziko lonse
la Edomu anaika maboma, ndipo Aedomu onse anasanduka anthu
a Davide. Ndipo Yehova anasunga Davide kuli konse anamukako.
15Ndipo Davide anakhala mfumu ya Aisrayeli onse, Davide
naweruza ndi cilungamo mirandu ya anthu onse. 16Ndipo Yoabu
mwana wa Zeruya anayang'anira ankhondo, ndi Josafati mwana
wa Ahiludi anali wolemba mbiri, 17ndi Zadoki mwana wa Ahitubi,
ndi Ahimeleki mwana wa Abyatara anali ansembe, ndi Seraya anali

mlembi. 18Ndipo Benaya mwana wa Jehoyada anayang'anira
Akereti ndi Apeleti. Ndipo ana a Davide anali nduna zace.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Davide acitira Mefiboseti mwana wa Jonatani cifundo

1Ndipo Davide anati, Kodi atsalako wina wa nyumba ya Sauli, kuti
ndimcitire cifundo cifukwa ca Jonatani? 2Ndipo panali mnyamata
wa m'nyumba ya Sauli dzina lace Ziba; ndipo anamuitana iye afike
kwa Davide; ndi mfumuyo inanena naye, Iwe ndiwe Ziba kodi? Nati
iye, Ndine mnyamata wanu ame. 3Ndipo mfumu inati, Kodi
atsalanso wina wa nyumba ya Sauli kuti ndimuonetsere cifundo ca
Mulungu? Ziba nanena ndi mfumu, Aliponso mwana wa Jonatani
wopunduka mapazi ace. 4Ndipo mfumu inanena naye, Ali kuti
iyeyo? Ziba nanena kwa mfumu, Onani ali m'nyumba ya Makiri,
mwana vya Amiyeli ku Lodebara. 5Pamenepo Davide anatumiza
anthu nakatenga iye ku nyumba ya Makiri mwana wa Amiyeli ku
Lodebara. 6Ndipo Mefiboseti mwana wa Jonatani, mwana wa Sauli,
anafika kwa Davide, nagwa nkhope yace pansi, namlambira. Ndipo
Davide anati, Mefiboseti! Nayankha iye, Ndine mnyamata
wanu. 7Ndipo Davide ananena naye, Usaopa, pakuti zoonadi
ndidzakucitira kukoma mtima cifukwa ca Jonatani atate wako; ndi
minda yonse ya Sauli ndidzakubwezera, ndipo udzadya pa gome
langa cikhalire. 8Ndipo iye anamlambira, nati, Mnyamata wanu
ndani, kuti mulikupenya garu wakufa monga ine. 9Pomwepo
mfumu inaitana Ziba, mnyamata wa Sauli, ninena naye, Za Sauli
zonse ndi za nyumba yace yonse ndampatsa mwana wa mbuye
wako. 10Ndipo uzimlimira munda wace, iwe ndi ana ako ndi
anyamata ako; nuzibwera nazo zipatso zace kuti mwana wa mbuye
wako akhale ndi zakudya; koma Mefiboseti, mwana wa mbuye
wako, adzadya pa gome langa masiku onse. Ndipo Ziba anali nao
ana amuna khumi ndi asanu, ndi anyamata makumi
awiri. 11Pomwepo Ziba anati kwa mfumu, Monga mwa zonse
mfumu mbuye wanga mulamulira mnyamata wanu, momwemo
adzacita mnyamata wanu. Tsono Mefiboseti, anadya pa gome la
Davide monga wina wa ana a mfumu. 12Ndipo Mefiboseti anali ndi
mwana wamwamuna wamng'ono, dzina lace ndiye Mika. Ndipo
onse akukhala m'nyumba ya Ziba anali anyamata a
Mefiboseti. 13Comweco Mefiboseti anakhala ku Yerusalemu, pakuti
anadya masiku onse ku gome la mfumu, ndipo anali wopunduka
mapazi ace onse awiri.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Davide akantha Aamoni ndi Aaramu

1Ndipo kunali zitapita izi, mfumu ya ana a Amoni inamwalira, ndipo Hanuni
mwana wace anakhala mfumu m'malo mwace. 2Ndipo Davide anati,
Ndidzacitira Hanuni mwana wa Nahasi zokoma, monga atate wace
anandicitira ine zokoma. Comweco Davide anatumiza ndi dzanja la anyamata
ace kuti akamsangalatse cifukwa ca atate wace. Ndipo anyamata a Davide
anafika ku dziko la ana a Amoni. 3Koma akalonga a ana a Amoni anati kwa
Hanuni mbuye wao, Kodi muganiza kuti Davide alemekeza atate wanu,
popeza anakutumizirani osangalatsa? Kodi Davide sanatumiza anyamata ace
kwa inu, kuti ayang'ane mudziwo ndi kuuzonda ndi kuupasula? 4Comweco
Hanuni anatenga anyamata a Davide nawameta ndebvu zao mbali imodzi,
nadula zobvala zao pakati, kufikira m'matako ao, nawaleka amuke. 5Pamene
anaciuza Davide iye anatumiza anthu kukakomana nao; pakuti amunawo
anacita manyazi akuru. Niti mfumu, Bakhalani ku Yeriko kufikira zamera
ndebvuzanu; zitameramubwere. 6Ndipo pamene ana a Amoni anazindikira
kuti anadzinunkhitsa kwa Davide, ana a Amoniwo anatumiza nadzilembera
Aaramu a ku Betirehobu, ndi Aaramu a ku Zoba, oyenda pansi zikwi makumi
awiri, ndi mfumu ya ku Maaka ndi anthu cikwi cimodzi, ndi anthu a mfumu ya
ku Tobu zikwi khumi ndi ziwiri. 7Ndipo pamene Davide anacimva, anatumiza
Yoabu ndi khamu lonse la anthu amphamvu. 8Ndipo ana a Amoni anaturuka,
nandandalitsa nkhondo polowera kucipata. Ndipo Aaramu a ku Zoba ndi a ku
Rehobu, ndi anthu a Tobu ndi Maaka, anali pa okha kuthengo. 9Ndipo pamene
Yoabu anaona kuti nkhondo inamdzera kumaso ndi kumbuyo, iye anasankha
amuna osankhidwa onse a Israyeli, nawandandalitsa ca kwa Aramu. 10Koma
anthu otsalawo anawapereka kwa Abisai mbale wace, amene
anawandandalitsa ca kwa Amoni. 11Ndipo iye anati, Aaramu akandipambana
ine, udzandithandiza ndiwe, koma ana a Amoni akapambana iwe, tsono
ndidzabwera ine kukuthandiza. 12Ulimbike mtima, ndipo ticite camuna lero
cifukwa ca anthu athu ndi midzi ya Mulungu wathu; Yehova nacite
comkomera. 13Comweco Yoabu ndi anthu amene anali naye anayandikira
kuponyana nkhondo ndi Aaramu. Ndipo iwowa anathawa pamaso
pace. 14Ndipo pamene ana a Amoni anaona kuti Aaramu anathawa, iwonso
anathawa pamaso pa Abisai, nalowa m'mudzimo. Ndipo Yoabu anabwera
kucokera kwa ana a Amoni, nafika ku Yerusalemu. 15Ndipo pamene Aaramu
anaona kuti Aisrayeli anawathyola, anasonkhana pamodzi. 16Ndipo
Hadarezeri anatumiza mthenga nakatenga Aaramu a ku tsidya la cimtsinje;
iwo nafika ku Helamu, ndi Sobaki kazembe wa khamu la nkhondo la
Hadarezeri anawatsogolera. 17Ndipo wina anauza Davide; iye nasonkhanitsa
Aisrayeli onse, naoloka Yordano nafika ku Helemu, Ndipo Aaramu
anandandalitsa nkhondo yao pa Davide namenyana naye. 18Ndipo Aaramu
anathawa pamaso pa Israyeli; Davide naphapo Aaramu apamagareta mazana
asanu ndi awiri, ndi apakavalo zikwi makumi anai, nakantha Sobaki kazembe
wa khamu lao, nafa iye pomwepo. 19Ndipo pamene mafumu onse, otumikira
Hadarezeri, anaona kuti Aisrayeli anawapambana, iwo anapangana mtendere
ndi Aisrayeli, nawatumikira, Comweco Aaramu anaopa kuwathandizanso ana a
Amoni.

Chimo loopsa la Davide

1Ndipo kunali pofikanso caka, nyengo yakuturuka mafumu, Davide
anatumiza Yoabu, pamodzi ndi anyamata ace, ndi Aisrayeli onse;
ndipo iwo anasakaza ana a Amoni, naumangira misasa yankhondo
Raba. Koma Davide anatsaliraku Yerusalemu.
2Ndipo kunali pa madzulo Davide anauka pa kama wace nayenda
pa tsindwi la nyumba ya mfumu. Ndipo iye ali patsindwipo anaona
mkazi alinkusamba; ndi mkaziyo anali wocititsa kaso
pomuyang'ana. 3Ndipo Davide anatumiza munthu nafunsa za
mkaziyo. Ndipo wina anati, Sindiye Bateseba, mwana wamkazi wa
Eliyamu mkazi wa Uriya Mhiti? 4Ndipo bavide anatumiza mithenga,
namtenga iye; iye nabwera kwa iye, ndipo anagona naye, pakuti
adacoka mumsambo; ndipo anabwereranso ku nyumba
yace. 5Ndipo mkaziyo anaima, natumiza munthu nauza Davide,
kuti, Ndiri ndi pakati. 6Davide natumiza kwa Yoabu, nati,
Unditumizire Uriya Mhiti. Ndipo Yoabu anatumiza Uriya kwa
Davide. 7Ndipo pakufika kwa iye Uriya uja, Davide anamfunsa kuti,
Yoabu ali bwanji? ndi anthu ali bwanji? ndi nkhondo iri
bwanji? 8Ndipo Davide anauza Uriya, Utsikire ku nyumba yako,
nutsuke mapazi ako, Ndipo Uriya anacoka ku nyumba ya mfumu,
ndipo anamtsata munthu ndi mphatso ya mfumu. 9Koma Uriya
anagona pa khomo la nyumba ya mfumu pamodzi ndi anyamata
onse a mbuye wace, osatsikira ku nyumba yace. 10Ndipo pamene
anauza Davide kuti, Uriya sanatsildra ku nyumba yace, Davide
ananena ndi Uriya, Kodi sunabwera kuulendo? cifukwa ninji
sunatsikira ku nyumba yako? 11Uriya nanena ndi Davide, Likasalo,
ndi Israyeli, ndi Yuda, alikukhala m'misasa, ndi mbuye wanga
Yoahu, ndi anyamata a mbuye wanga alikugona kuthengo, potero
ndikapita ine kodi ku nyumba yanga kuti ndidye, ndimwe, ndigone
ndi mkazi wanga? Pali inu, pali moyo wanu, sindidzacita
cinthuci. 12Ndipo Davide anati kwa Uriya, Utsotse pane leronso,
ndipo mawa ndidzakulola umuke, Comweco Uriya anakhala ku
Yerusalemu tsiku lomwelo ndi m'mawa mwace. 13Ndipo
pakumuitana Davide, iyeyo anadya namwa pamaso pace; Davide
namledzeretsa; ndipo usiku anaturuka kukagona pa kama wace
pamodzi ndi anyamata a mbuye wace; koma sanatsildra ku
nyumba yace. 14Ndipo m'mawa Davide analembera Yoabu kalata,
wopita nave Uriya. 15Ndi m'kalatamo analemba kuti, Mumuike
Uriya pa msongwe wa nkhondo yolimba, ndipo mumlekerere kuti
akanthidwe nafe. 16Ndipo Yoabu atayang'anira mudziwo, anaika
Uriye pomwe anadziwa kuti pali ngwazi. 17Ndipo akumudziwo
anaturuka, namenyana ndi Yoabu; ndipo adagwapo anthu ena,
ndiwo a anyamata a Davide; ndi Uriya Mhiti anafanso. 18Pamenepo

Yoabu anatumiza munthu nauza Davide zonse za
nkhondoyi; 19nauza mthengawo kuti, Utatsiriza kuuza mfumu
zonse za nkhondozo; 20kudzali kuti ukapsa mtima wa mfumu nikati
kwa iwe, Cifukwa ninji munayandikira pafupi potere pamudzi
kukamenyana nao? Simunadziwa kodi kuti apalingawo
adzaponya? 21Ndani anakantha Abimeleki mwana wa Jerubeseti?
Sadamponyera kodi mphero mkazi wa palinga nafa iye ku Tebezi?
Munasendera bwanji pafupi potere pa lingalo? Tsono udzanena,
Mnyamata wanu Uriya Mhiti, iyenso adafa, 22Comweco mthengawo
unamuka, nufika, nudziwitsa Davide zonse Yoabu
anamtumiza. 23Ndipo mthengawo unati kwa Davide, Anthuwo
anatilaka naturukira kwa ife kumundako, koma tinawa gwera
kufikira polowera kucipata, 24Ndipo akuponyawo amene anali
palinga anaponya anyamata anu; ndipo anyamata ena a mfumu
anafa, ndi mnyamata wanu Uriya Mhiti, iyenso anafa. 25Pomwepo
Davide ananena ndi mthengawo, Udzatero kwa Yoabu, Cisakuipire
ici, lupanga limaononga ina ndi mnzace. Onjeza kulimbitsa
nkhondo yako pamudzipo, nuupasule; numlimbikitse
motere. 26Ndipo pamene mkazi wa Uriya anamva kuti Uriya
mwamuna wace adamwalira, iye analira maliro a mwamuna
wace. 27Ndipo pakuturuka malirowo, Davide anatumiza munthu
namtenga afike kwao ku nyumba yace; ndipo iyeyo anakhala
mkazi wace nambalira mwana wamwamuna. Koma Yehova
anaipidwa ndi cinthu cimene Davide adacita.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Kulapa ndi kulangidwa kwa Davide

1Ndipo Yehova anatumiza Natani kwa Davide. Ndipo anafika kwa
iye nanena naye, Pa mudzi wina panali anthu awiri; wina
wolemera, wina wosauka. 2Wolemerayo anali nazo zoweta
zazing'ono ndi zazikuru zambiri ndithu; 3koma wosaukayo analibe
kanthu kena koma kamwana kakakazi ka nkhosa, kamene
anakagula ndi kukaweta; ndipo kameneko kanakula naye pamodzi
ndi ana ace. Kanadyako cakudya cace ca iye yekha, kanamwera
m'cikho ca iye yekha, kanagona pa cifukato cace, ndipo kanali kwa
iye ngati mwana wace wamkazi. 4Ndipo kwa wolemerayo kunafika
mlendo, ndipo iye analeka kutengako mwa zoweta zace zazing'ono
ndi zazikuru, kuphikira mlendo amene anafika kwa iye, koma
anatenga mwana wa nkhosa wa wosaukayo, naphikira munthu
amene anafika kwa iye. 5Pamenepo mkwiyo wa Davide unayaka
ndithu pa munthuyo, nati kwa Natani, Pali Yehova, munthu amene
anacita ici, ayenera kumupha; 6ndipo adzabwezera mwa mwana
wa nkhosayo ena anai, cifukwa anacita ici osakhala naco cifundo.
7Ndipo Natani ananena kwa Davide, Munthuyo ndi inu nomwe.
Atero Yehova, Mulungu wa Israyeli, Ndinakudzoza ukhale mfumu ya
Israyeli, ndinakupulumutsa m'dzanja la Sauli; 8ndinakupatsa
nyumba ya mbuye wako, ndi akazi a mbuye wako pa cifukato cako,
ndinakupatsanso nyumba ya Israyeli ndi ya Yuda; ndipo zimenezi
zikadakucepera ndikadakuonjezera zina zakuti zakuti. 9Cifukwa
ninji unapeputsa mau a Yehova ndi kucita cimene ciri coipa
pamaso pace? Unakantha Uriya Mhiti ndi lupanga ndi kutenga
mkazi wace akhale mkazi wako; ndipo unamupha iye ndi lupanga
la ana a Amoni. 10Cifukwa cace tsono lupanga silidzacoka pa
nyumba yako nthawi zonse, popeza unandipeputsa Ine,
nudzitengera mkazi wa Uriya Mhiti akhale mkazi wako. 11Atero
Yehova, Taona ndidzakuutsira zoipa, zobadwa m'nyumba yako ya
iwe wekha; ndipo ndidzacotsa akazi ako pamaso pako ndi
kuwapatsa mnansi wako, amene adzagona ndi akazi ako dzuwa liri
denene. 12Pakuti iwe unacicita m'tseri; koma Ine ndidzacita cinthu
ici pamaso pa Aisrayeli onse, dzuwa liri nde. 13Ndipo Davide anati
kwa Natani, Ndinacimwira Yehova. Natani nati kwa Davide,
Ndiponso Yehova wacotsa chimo lanu, simudzafa. 14Koma popeza
pakucita ici munapatsa cifukwa cacikuru kwa adani a Yehova ca
kucitira mwano, mwanayonso wobadwira inu adzafa
ndithu. 15Ndipo Natani anamuka kwao. Ndipo Yehova anadwaza
mwana amene mkazi wa Uriya anambalira Davide, nadwala
kwambiri. 16Cifukwa cace Davide anapempherera mwanayo kwa
Mulungu; Davide nasala kudya, nalowa, nagona usiku wonse
pansi. 17Ndipo akuru a m'nyumba yace ananyamuka, naima pa iye,

kuti akamuutse pansi; koma anakana, osafuna kudya nao. 18Ndipo
tsiku lacisanu ndi ciwiri mwanayo anamwalira. Ndipo anyamata a
Davide anaopa kumuuza kuti mwanayo wafa, pakuti iwo anati,
Onani, mwanayo akali moyo, tinalankhula naye, osamvera mau
athu; tsono tidzamuuza bwang kuti mwana wafa; sadzadzicitira
coipa nanga? 19Koma pamene Davide anaona anyamata ace
alikunong'onezana, Davide anazindikira kuti mwanayo adafa;
Davide nanena ndi anyamata ace, Kodi mwanayo wafa? Nati iwo,
Wafa. 20Pamenepo Davide ananyamuka pansi, nasamba, nadzola,
nasintha zobvala; nafika ku nyumba ya Yehova, napembedza;
pamenepo anafika ku nyumba yace; ndipo powauza anamuikira
cakudya, nadya iye. 21Pamenepo anyamata ace ananena naye, Ici
mwacita nciani? Mwanayo akali moyo, munasala kudya ndi
kumlira, koma pakufa mwanayo munyamuka ndi kudya, 22Nati iye,
Pamene mwanayo akali ndi moyo, ndinasala kudya ndi kulira,
pakuti ndinati, Adziwa ndani kapena Yehova adzandicitira cifundo
kuti mwanayo akhale ndi moyo. 23Koma tsopano wafa,
ndidzasaliranjinso kudya? Kodi ndikhoza kumbweza? Ine
ndidzamuka kuli iye, koma iye sadzabweranso kwa ine.

Kubadwa kwa Solomo

24Ndipo Davide anasangalatsa Bateseba mkazi wace, nalowa kwa
iye, nagona naye; ndipo anabala mwana wamwamuna, namucha
dzina lace Solomo. Ndipo Yehova anamkonda iye, 25natumiza ndi
dzanja la Natani mneneriyo, namucha dzina lace Wokondedwa ndi
Yehova, cifukwa ca Yehova.

26Ndipo Yoabu anathira nkhondo pa Raba wa ana a Amoni, nalanda
mudzi wacifumu. 27Yoabu natumiza mithenga kwa Davide nati,
Ndaponyana ndi Raba, inde ndalanda mudzi wa
pamadzi. 28Cifukwa cace tsono musonkhanitseanthu otsalawo,
nimumangire mudziwo zithando, muulande; kuti ine ndingalande
mudziwo, ndipo ungachedwe ndi dzina langa. 29Ndipo Davide
anasonkhanitsa anthu onse, napita ku Raba, naponyana nao,
naulanda. 30Nacotsa korona pa mutu wa mfumu yao; kulemera
kwace kunali talente wa golidi; ndipo m'menemo munali miyala ya
mtengo wapatali; ndipo anamuika pa mutu wa Davide. Iye
naturutsa zofunkha za mudziwo zambirimbiri. 31Naturutsa anthu a
m'mudzimo, nawaceka ndi mipeni ya mana mano, ndi nkhwangwa
zacitsulo; nawapsitiriza ndi citsulo, nawapititsa m'ng'anjo
yanjerwa; natero ndi midzi yonse ya ana a Amoni. Ndipo Davide
ndi anthu onse anabwerera kumka ku Yerusalemu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Chimo loopsa la Amnoni

1Ndipo kunali citapita ici, popeza Abisalomu mwana wa Davide
anali naye mlongo wace wokongola, dzina lace ndiye Tamara,
Amnoni mwana wa Davide anamkonda iye. 2Ndipo Amnoni
anapsinjikadi nayamba kudwala cifukwa ca mlongo wace Tamara,
pakuti anali namwali, ndipo Amnoni anaciyesa capatali kumcitira
kanthu. 3Koma Amnoni anali ndi bwenzi lace, dzina lace ndiye
Jonadabu, mwana wa Sineya, mbale wa Davide. Ndipo Jonadabu
anali munthu wocenjera ndithu. 4Nanena naye, Iwe mwana wa
mfumu, uonderanji tsiku ndi tsiku? Sungandiuze kodi? Ndipo
Amnoni anati kwa iye, Ndikonda Tamara, mlongo wa mbale wanga
Abisalomu. 5Ndipo Jonadabu ananena naye, Ugone pa kama wako
ndi kudzikokomeza ulikudwala; ndipo pamene atate wako
akadzakuona unene naye, Mulole mlongo wanga Tamara abwere
kundipatsa kudya, nakonzere cakudyaco pamaso panga kuti
ndicione ndi kucidya ca m'manja mwace. 6Comweco Amnoni
anagona, nadzikokomeza alikudwala; ndipo pamene mfumu inadza
kumuona, Amnoni anati kwa mfumuyo, Mulole Tamara mlongo
wanga abwere ndi kundipangira timitanda tiwiri pamaso panga,
kuti ndikadye ca m'manja mwace. 7Ndipo Davide anatumiza mau
kwao kwa Tamara, kuti, Upite ku nyumba ya mlongo wako Amnoni,
numkonzere cakudya, 8Comweco Tamara anapita ku nyumba ya
mlongo wace Amnoni; ndipo iye anali cigonere. Ndipo anatenga
ufa naukanda naumba timitanda pamaso pace, nakazinga
timitandato. 9Ndipo anatenga ciwaya natiturutsa pamaso pace;
koma anakana kudya. Ndipo Amnoni anati, Anthu onse aturuke
kundisiya ine. Naturuka onse, kumsiya. 10Ndipo Amnoni anati kwa
Tamara, Bwera naco cakudya kucipinda kuti ndikadye ca m'manja
mwako. Ndipo Tamara anatenga timitanda anatipangato, nabwera
nato kucipinda kwa Amnoni mlongo wace. 11Ndipo pamene
anabwera nato pafupi kuti adye, iye anamgwira, nanena naye, Idza
nugone nane, mlongo wanga. 12Koma iye anamyankha nati, lai,
mlongo wanga, usandicepetsa ine, pakuti cinthu cotere siciyenera
kucitika m'Israyeli, usacita kupusa kumeneku. 13Ndipo ine,
manyazi anga ndidzapita nao kuti? ndipo iwenso udzakhala ngati
wina wa zitsiru m'Israyeli. Cifukwa cace tsono ulankhule ndi
mfumu; iyeyu sadzakukaniza ine. 14Koma iye sadafuna kumvera
mau ace, ndipo popeza anali wamphamvu ndi iye,
anamkangamiza, nagona naye. 15Atatero Amnoni anadana naye
ndi cidani cacikuru kopambana; pakuti cidani cimene anamuda
naco, cinali cacikuru koposa cikondi adamkonda naco. Ndipo
Amnoni ananena naye, Nyamuka, coka. 16Koma iye ananena naye,
Usamatero, pakuti coipa ici cakuti ulikundipitikitsa ncacikuru

coposa cina cija unandicitira ine. Kama anakana kumvera. 17Pomwepo anaitana mnyamata wace amene anamtumikira, nati, Turutsa mkazi uyu kwa ine, nupiringidze citseko atapita iye. 18Ndipo iye anabvala cobvala ca mawanga mawanga, popeza ana akazi a mfumu okhala anamwali amabvala zotere. Ndipo mnyamata wace anamturutsa, napiringidza citseko atapita iye. 19Ndipo Tamara anathira phulusa pamutu pace, nang'amba cobvala ca mawanga mawanga cimene analikubvala, nagwira dzanja lace pamutu pace, namuka nayenda, nalira komveka. 20Ndipo Abisalomu mlongo wace ananena nave, Kodi mlongo wako Arononi anali ndi iwe? Koma tsopano ukhale cete, mlongo wanga, iye ali mlongo wako; usabvutika ndi cinthuci. Comweco Tamara anakhala wounguruma m'nyumba ya Abisalomu mlongo wace. 21Koma pamene mfumu Davide anamva zonsezi, anakwiya ndithu. 22Ndipo Abisalomu sanalankhula ndi Arononi cabwino kapena coipa, pakuti Abisalomu anamuda Amnoni, popeza adacepetsa mlongo wace Tamara.
23Ndipo zitapita zaka ziwiri zathunthu, kunali kuti Abisalomu anali: nao osenga nkhosa zace ku Baalahazore pafupi pa Efraimu; ndipo Abisalomu anaitana ana amuna onse a mfumu. 24Abisalomu nafika kwa mfumu nati, Onani, ine mnyamata, wanu ndiri nao osenga nkhosa; inu mfumu ndi anyamata anu mupite nane mnyamata wanu. 25Ndipo mfumu inati kwa Abisalomu, lai mwana wanga, tisapite tonse, kuti tingakucurukire. Ndipo iye anaiumirira koma inakana kupita; koma inamdalitsa. 26Pomwepo Abisalomu anati, Ngati nkutero, mulole mbale wanga Amnoni apite nafe. Ndipo mfumu inanena naye, iye apitirenji nawe? 27Koma Abisalomu anaiumirira iyo, nilola kuti Amnoni ndi ana amuna onse a mfumu apite naye. 28Ndipo Abisalomu anakamulira anyamata ace, nati, Inu mukhale maso, mtima wa Amnoni ukasekera ndi vinyo, ndipo ine ndikati kwa inu, Kanthani Amnoni; pamenepo mumuphe, musaope; sindine ndakulamulirani inu mulimbike, citani camuna. 29Ndipo anyamata a Abisalomu anamcitira Amnoni monga umo Abisalomu anawalamulira. Pomwepo ana amuna onse a mfumu ananyamuka, nakwera munthu yense pa nyuru yace, nathawa. 30Ndipo kunali akali panjira, mau anafika kwa Davide, kuti, Abisalomu anapha ana amuna onse a mfumu, osatsalapo ndi mmodzi yense. 31Pamenepo mfumu inanyamuka ning'amba zobvala zace nigona pansi, ndipo anyamata ace onse anaimirirapo ndi zobvala zao zong'ambika. 32Ndipo Jonadabu mwana wa Simeya mbale wa Davide anayankha nati, Mbuye wanga asaganize kuti anapha anyamata onse, ana amuna a mfumu, pakuti Amnoni yekha wafa, pakuti Ici cinatsimikizika ndi mau a Abisalomu kuyambira tsiku lija anacepetsa mlongo: wace Tamara. 33Cifukwa

cace tsono mfumu mbuye wanga asasauke mtima ndi cinthuci, ndi kuganiza kuti ana amuna onse a mfumu afa; pakuti Amnoni yekha wafa. 34Koma Abisalomu anathawa. Ndipo mnyamata wakudikira anatukula maso ace nayang'ana, ndipo onani, m'mbuyo mwace anthu ambiri analikubwera m'njira yolambalala phiri. 35Ndipo Jonadabu ananena ndi mfumu, Onani, ana amuna a mfumu afika; monga ananena mnyamata wanu, momwemo. 36Ndipo kunali pakutsiriza iye kulankhula, onani, pomwepo ana amuna a mfumu anafika, nakweza mau ao, nalira misozi; ndi mfumu yomwe ndi anyamata ace analira ndi kulira kwakukuru ndithu. 37Koma Abisalomu anathawa, nanka kwa Talimai mwana wa Amihuri mfumu ya ku Gesuri. Ndipo Davide analira mwana wace tsiku ndi tsiku.
38Comweco anathawa Abisalomu, nanka ku Gesuri, nakakhala kumeneko zaka zitatu. 39Ndipo mfumu Davide analira kunka kwa Abisalomu, cifukwa anasangalatsidwa pa imfa ya Amnoni.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Abisalomu abwera ku Yerusalemu

1Ndipo Yoabu mwana wa Zeruya anazindikira kuti mtima wa
mfumu unalunjika kwa Abisalomu. 2Ndipo Yoabu anatumiza ku
Tekowa, natenga kumeneko mkazi wanzeru, nanena naye,
Ukokomezeke monga mfedwa, nubvale zobvala za pamaliro,
osadzola mafuta, koma ukhale ngati munthu wamkazi wakulira
akufa nthawi yaikuru. 3Nulowe kwa mfumu, nulankhule nayo
monga momwemo. Comweco Yoabu anampangira mau. 4Ndipo
pamene mkazi wa ku Tekowayo anati alankhule ndi mfumuyo,
anagwa nkhope yace pansi namlambira, nati, Ndithandizeni
mfumu. 5Ndipo mfumuyo inanena naye, Usowanji? iye nayankha,
Zoonadi ine ndine mkazi wamasiye, mwamuna wanga ana
mwalira. 6Ndipo mdzakazi wanu ndinali nao ana amuna awiri,
ndipo awiriwa analimbana kumunda, panaboo wina wakuwaletsa,
koma wina anakantha mnzace namupha. 7Ndipo onani, cibale
conse cinaukira mdzakazi wanu, ndi kuti, Upereke iye amene
anakantha mbale wace, kuti timuphe cifukwa ca moyo wa mbale
wace amene anamupha; koma pakutero adzaononga wolowa
yemwe; comweco adzazima khara langa lotsala, ndipo sadzasiyira
mwamuna wanga dzina kapena mbeu kunja kuno. 8Ndipo mfumu
inanena ndi mkaziyo, Pita ku nyumba yako, ndipo ndidzalamulira
za iwe. 9Ndipo mkazi wa ku Tekowayo ananena ndi mfumu, Mbuye
wanga mfumu, mphulupulu ikhale pa ine ndi pa nyumba ya atate
wanga; ndipo mfumu ndi mpando wacifumu wao zikhale zopanda
cifukwa. 10Ndipo mfumu inati, Ubwere naye kwa ine ali yense
wakunena kanthu ndi iwe, ndipo iyeyo sadzakukhudzanso. 11Nati
iye, Mfumu mukumbukile Yehova Mulungu wanu kuti wolipsa
mwazi asaonjeze kuononga, kuti angaononge mwana wanga. Niti
iyo, Pali Yehova, palibe tsitsi limodzi la mwana wako lidzagwa
pansi. 12Pamenepo mkaziyo anati, Mulole mdzakazi wanu
alankhule mau kwa mbuye wanga mfumu. Niti Iyo, Nena. 13Ndipo
mkaziyo anati, Cifukwa ninjinso munalingalira cinthu cotere pa
anthu a Mulungu? pakuti pakulankhula mau awa mfumu ikunga
woparamula, popeza mfumu siitumiza okamtenganso woingidwa
wace. 14Pakuti kufa tidzafa, ndipo tiri ngati madzi otayika pansi
amene sakhoza kuwaolanso; ngakhale Mulungu sacotsa moyo,
koma alingalira ngra yakuti wotayikayo asakhale womtayikira
iye. 15Cifukwa cace tsono cakuti ndadzanena mau awa ndi mbuye
wanga mfumu, ndico kuti anthu anandiopsa ine; ndipo mdzakazi
wanu ndinati, Ndilankhuletu ndi mfumu; kapena mfumu idzacita
copempha mdzakazi wace. 16Pakuti mfumu idzamvera ndi
kupulumutsa mdzakazi wace m'dzanja la munthu wakufuna
kundiononga ine pamodzi ndi mwana wanga, kuticotsa ku colowa

ca Mulungu. 17Ndipo mdzakazi wanu ndinati, Mau a mbuye wanga mfumu akhale opumulitsa; mbuye wanga mfumu ali ngati mthenga wa Mulungu, kuzindikira zabwino ndi zoipa; ndipo Yehova Mulungu wanu akhale nanu. 18Pamenepo mfumu inayankha, ninena naye mkaziyo, Usandibisire kanthu ka zimene ndidzakufunsa iwe. Mkaziyo nati, Mbuye wanga mfumu anene. 19Ndipo mfumuyo inati, Kodi Yoabu adziwana ndi iwe mwa izi zonse? Mkaziyo nayankha nati, Pali moyo wanu mbuye wanga mfumu, palibe kulewa ku dzanja lamanja, kapena kulamanzere kwa zonse mudazinena mbuye wanga mfumu; pakuti mnyamata wanu Yoabu ndiye anandiuza, naika mau onse awa m'kamwa mwa mdzakazi wanu. 20Mnyamata wanu Yoabu anacita cinthu ici kuti asandulize mamvekedwe a mranduwo. Ndipo mbuye wanga ali wanzeru, monga ndi nzeru ya mthenga wa Mulungu, kudziwa zonse ziri m'dziko lapansi. 21Ndipo mfumuyo inanena ndi Yoabu, Taonatu, ndacita cinthu ici; cifukwa cace, pita nubwere nayenso mnyamatayo Abisalomu. 22Ndipo Yoabu anagwa nkhope yace pansi, namlambira, nadalitsa mfumuyo; nati Yoabu, Lero mnyamata wanu ndadziwa kuti munandikomera mtima, mbuye wanga mfumu, popeza mfumu yacita copempha mnyamata wace. 23Comweco Yoabu ananyamuka namka ku Gesuri, nabwera naye Abisalomu ku Yerusalemu. 24Ndipo mfumu inati, Apambukire ku nyumba yaiye yekha, koma asaone nkhope yanga. Comweco Abisalomu anapambukira ku nyumba ya iye yekha, wosaona nkhope ya mfumu.
25Ndipo m'Israyeli monse munalibe wina anthu anamtama kwambiri cifukwa ca kukongola kwace monga Abisalomu; kuyambira ku mapazi kufikira pakati pa mutu wace mwa iye munalibe cirema. 26Ndipo pometa tsitsi lace amameta potsiriza caka, cifukwa tsitsi linamlemerera, cifukwa cace atalimeta anayesa tsitsi la pa mutu wace, napeza masekeli mazana awiri, monga mwa muyeso wa mfumu. 27Ndipo kwa Abisalomu kunabadwa ana amuna atatu ndi mwana wamkazi mmodzi, dzina lace ndiye Tamara, iye ndiye mkazi wokongola nkhope.
28Ndipo Abisalomu anakhala ku Yerusalemu zaka ziwiri zathunthu, osaona nkhope ya mfumu. 29Pamenepo Abisalomu anaitana Yoabu kuti akamtumize iye kwa mfumu; koma anakana kubwera kwa iye; ndipo anamuitananso nthawi yaciwiri, koma anakana kubwera. 30Cifukwa cace iye anati kwa anyamata ace, Onani munda wa Yoabu uli pafupi ndi wanga, ndipo iye ali ndi barele pamenepo, mukani mukamtenthere. Ndipo anyamata a Abisalomu anatentha za m'mundawo. 31Pamenepo Yoabu ananyamuka nafika kwa Abisalomu ku nyumba yace, nanena naye, Cifukwa ninji anyamata anu anatentha za m'munda mwanga; 32Abisalomu

nayankha Yoabu, Ona, ndinatumiza kwa iwe kuti, Bwera kuno kuti ndikutume kwa mfumu kukanena, Ine ndinabwereranji kucokera ku Gesuri? mwenzi nditakhala komweko; cifukwa cace tsono mundilole kuona nkhope ya mfumu; ndipo ngati mulinso mphulupulu mwa ine andiphe ndithu. 33Comweco Yoabu anadza kwa mfumu namuuza; ndipo pamene iye adaitana Abisalomu, iye anadza kwa mfumu naweramira nkhope yace pansi pamaso pa mfumu; ndipo mfumu inampsompsona Abisalomu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Kupanduka kwa Abisalomu, ndi kuthawa kwa Davide

1Ndipo kunali, citapita ici Abisalomu anadzikonzera gareta ndi
akavalo ndi anthu makumi asanu akuthamanga
momtsogolera. 2Ndipo Abisalomu analawirira, nakaima pa njira ya
kucipata; ndipo kunatero, pakakhala munthu ali yense ndi mrandu
woyenera kufika kwa mfumu kuti aweruze, Abisalomu anamuitana,
nati, Ndinu wa ku mudzi uti? Ndipo anati, Mnyamata wanu; ndiye
wa pfuko tina la Aisrayeli. 3Abisalomu nanena naye, Ona zokamba
zako ndizo zabwino ndi zolungama; koma mfumu sinauze wina kuti
adzamve za iwe. 4Abisalomu anatinso, Mwenzi atandiika ine
ndikhale woweruza m'dzikomo, kuti munthu yense amene ali ndi
mrandu wace kapena cifukwa cace, akadafika kwa ine; ndipo
ndikadamcitira zacilungamo! 5Ndipo kunatero kuti pakusendera
munthu ali yense kudzamlambira, iye anatambasula dzanja lace,
namgwira, nampsompsona. 6Abisalomu anacitira zotero Aisrayeli
onse akudza kwa mfumu kuti aweruze mrandu wao; comweco
Abisalomu anakopa mitima ya anthu a Israyeli.
7Ndipo kunali pakutha zaka zinai Abisalomu ananena kwa mfumu,
Mundilole ndimuke ku Hebroni ndikacite cowinda canga
ndinaciwindira Yehova. 8Pakuti mnyamata wanu ndinawinda
pakukhala ine ku Gesuri m'Aramu, ndi kuti, Yehova
akadzandibwezeranso ndithu ku Yerusalemu, ine ndidzatumikira
Yehova. 9Ndipo mfumu inanena naye, Muka ndi mtendere.
Comweco ananyamuka, nanka ku Hebroni. 10Koma Abisalomu
anatumiza ozonda ku mafuko onse a Israyeli, kuti, Pakumva kulira
kwa lipenga, pomwepo muzinena, Abisalomu ali mfumu ku
Hebroni. 11Ndipo pamodzi ndi Abisalomu panapita anthu mazana
awiri a ku Yerusalemu ndiwo oitanidwa, namuka m'kupulukira
kwao, osadziwa kanthu. 12Ndipo Abisalomu anaitana Ahitofeli
Mgiloni, mphungu wa Davide, ku mudzi wace ndiwo Gilo, pamene
iye analikupereka nsembe. Ndipo ciwembuco cinali colimba; pakuti
anthu anacurukacurukabe kwa Abisalomu.
13Ndipo mthenga unafika kwa Davide nuti, Mitima ya anthu a
Israyeli itsata Abisalomu. 14Ndipo Davide ananena nao anyamata
ace onse akukhala naye ku Yerusalemu, Nyamukani tithawe,
tikapanda kuthawa palibe mmodzi wa ife adzapulumuka
Abisalomu; fulumirani kucoka, angatipeze msanga ndi
kutigwetsera zoipa ndi kukantha mudzi ndi lupanga
lakuthwa. 15Ndipo anyamata a mfumu ananena kwa mfumu,
Onani, monga mwa zonse mbuye wathu mfumu adzasankha,
anyamata anu ndife. 16Mfumu nituruka, ndi banja lace lonse
tinamtsata. Ndipo mfumu inasiya akazi khumi ndiwo akazi ang'ono,
kusunga nyumbayo. 17Ndipo mfumu inaturuka, ndi anthu onse

anamtsata; naima ku nyumba ya payokha. 18Ndipo anyamata ace
onse anapita naye limodzi; ndi Akereri ndi Apeleti, ndi Agiti onse,
anthu mazana asanu ndi limodzi omtsata kucokera ku Gati, anapita
pamaso pa mfumu. 19Pomwepo mfumu inanena kwa Itai Mgiti,
Bwanji ulikupita nafe iwenso? Ubwerere nukhale ndi mfumu; pakuti
uli mlendo ndi wopitikitsidwa; bwerera ku malo a iwe
wekha. 20Popeza unangofika dzulo lokha, kodi ndidzakutenga lero
kuyendayenda nafe popeza ndipita pomwe ndiona popita?
ubwerere nubwereretsenso abale ako; cifundo ndi zoonadi zikhale
nawe. 21Itai nayankha mfumu nuti, Pali Yehova, pali mbuye wanga
mfumu, zoonadi apo padzakhala mbuye wanga mfumu, kapena
mpa imfa kapena mpa moyo, pomwepo padzakhalanso mnyamata
wanu. 22Ndipo Davide ananena ndi Itai, Tiye nuoloke. Ndipo Itai
Mgiti anaoloka, ndi anthu ace onse, ndi ana ang'ono onse amene
anali naye. 23Ndipo dziko lonse linalira ndi mau okweza; ndipo
anthu onse anaoloka, ndi mfumu yomwe inaoloka mtsinje wa
Kidroni, ndipo anthu onse anaolokera ku njira ya kucipululu.

Zadoki ndi Abyatara abwerera ndi likasa ku Yerusalemu

24Ndipo onani, Zadoki yemwe anadza, ndi Alevi onse pamodzi
naye, alikunyamula likasa la cipangano la Mulungu; natula likasa la
Mulungu; ndi Abyatara anakwera kufikira anthu onse anatha
kuturuka m'mudzimo. 25Ndipo mfumu inanena ndi Zadoki,
Ubwererenalo likasa la Mulungu kumudziko; akandikomera mtima
Yehova, iye adzandibwezanso, nadzandionetsanso gi, ndi pokhala
pace pomwe. 26Koma iye akatero kuti, Sindikondwera nawe konse;
onani, ndine pano, andicitire cimene cimkomera. 27Ndipo mfumu
inanenanso ndi Zadoki wansembeyo, Suli mlauli kodi? ubwere
kumudzi mumtendere pamodzi ndi ana ako amuna awiri, Ahimaazi
mwana wako ndi Jonatani mwana wa Abyatara. 28Ona ndidzaima
pa madooko a m'cipululu kufikira afika mau ako akunditsimikizira
ine. 29Cifukwa cace Zadoki ndi Abyatara ananyamulanso likasa la
Mulungu nafika nalo ku Yerusalemu. Ndipo iwo anakhala
kumeneko.

30Ndipo Davide anakwera pa cikweza ca ku Azitona nakwera nalira
misozi; ndipo anapfunda mutu wace nayenda ndi mapazi osabvala;
ndi anthu onse amene anali naye anapfunda munthu yense mutu
wace, ndipo anakwera, nalira misozi pokwerapo. 31Ndipo wina
anauza Davide nati, Ahitofeli ali pakati pa opangana ciwembu
pamodzi ndi Abisalomu. Davide nati, Yehova, musandulize
uphungu wa Ahitofeli ukhale wopusa. 32Ndipo kunali pakufika
Davide ku mutu wa phiri, kumene amapembedza Mulungu, onani,
Husai M-ariki anadzakomana naye ali ndi maraya ace ong'ambika,
ndi dothi pamutu pace. 33Ndipo Davide ananena naye, Ukapita
pamodzi ndi ine udzandilemetsa; 34koma ukabwerera kumudzi, ndi

kunena ndi Abisalomu, Ine ndine mnyamata wanu, mfumu; monga kale ndinali mnyamata wa atate wanu, momwemo tsopano ndidzakhala mnyamata wanu; pomwepo udzanditsutsira uphungu wa Ahitofeli. 35Ndipo suli nao kumeneko Zadoki ndi Abyatara ansembewo kodi? motero ciri conse udzacimva ca m'nyumba ya mfumu uziuza Zadoki ndi Abyatara ansembewo. 36Onani, ali nao komweko ana amuna ao awiri, Ahimaazi mwana wa Zadoki, ndi Jonatani mwana wa Abyatara; iwowa muwatumize kuti adzandiuze ciri conse mudzacimva. 37Comweco Husai bwenzi la Davide anadza m'mudzimo; ndipo Abisalomu anafika ku Yerusalemu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Davide akomana ndi Ziba. Simeyi amtukwana

1Ndipo pamene Davide anapitirira pang'ono pamutu pa phiri,
onani, Ziba mnyamata wa Mefiboseti anakomana naye, ali nao
aburu awiri omanga mbereko, ndi pamenepo mitanda ya mikate
mazana awiri, ndi ncinci zamphesa zana limodzi, ndi zipatso za
m'dzinja zana limodzi, ndi thumba la vinyo. 2Ndipo mfumu inanena
ndi Ziba, Ulikutani ndi zimenezi? Nati Ziba, Aburuwo ndiwo kuti
akaberekepo a pa banja lanu; ndi mitanda ya mikate ndi zipatso za
m'dzinja ndizo zakudya za anyamata; ndi vinyoyo akufoka
m'cipululu akamweko. 3Ndipo mfumu inati, Mwana wa mbuye wako
ali kuti? Ziba nanena ndi mfumu, Onani, akhala ku Yerusalemu;
pakuti anati, Lero nyumba ya Israyeli idzandibwezera ufumu wa
atate wanga. 4Pomwepo mfumu inanena ndi Ziba, Ona, za
Mefiboseti zonse ziri zako. Ndipo Ziba anati, Ndikulambirani,
mundikomere mtima, mbuye wanga mfumu.
5Ndipo pakufika mfumu Davide ku Bahurimu, onani, panaturuka
pamenepo munthu wa banja la nyumba ya Sauli, dzina lace ndiye
Simeyi, mwana wa Gera; iyeyu anaturukako, nayenda
natukwana. 6Ndipo iye anaponya miyala Davide ndi anyamata
onse a mfumu Davide, angakhale anthu onse ndi ngwazi zonse
zinali kudzanja lamanja ndi ku dzanja lamanzere kwace. 7Ndipo
anatero Simeyi pakutukwana, Coka, coka, munthu wa mwazi iwe,
woipa iwe; 8Yehova wabwezera pa iwe mwazi wonse wa nyumba
ya Sauli, amene iwe wakhala mfumu m'malo mwace; ndipo Yehova
wapereka ufumuwo m'dzanja la Abisalomu mwana wako; ndipo
ona, wagwidwa m'kuipa kwako kwa iwe wekha, cifukwa uli munthu
wa mwazi. 9Pomwepo Abisai mwana wa Zeruya ananena ndi
mfumu, Garu wakufa uyu atukwaniranji mbuye wanga mfumu?
Mundilole ndioloke ndi kudula mutu wace. 10Mfumu niti, Ndiri ndi
ciani ndi inu, ana a Zeruya? Pakuti atukwana, ndi pakuti Yehova
ananena naye, Utukwane Davide; ndani tsono adzanena, Watero
cifukwa ninji? 11Ndipo Davide ananena ndi Abisai ndi anyamata
ace onse, Onani, mwana wanga woturuka m'matumbo anga,
alikufuna moyo wanga; koposa kotani nanga Mbenjamini uyu?
mlekeni, atukwane, pakuti Yehova anamuuza. 12Kapena Yehova
adzayang'anira cosayeneraci alikundicitira ine, ndipo Yehova
adzandibwezera cabwino m'malo mwa kunditukwana kwa
lero. 13Comweco Davide ndi anthu ace anapita m'ngra, ndipo
Simeyi analambalala paphiri popenyana naye, namuka natukwana,
namponya miyala, nawaza pfumbi, 14Ndipo mfumu ndi anthu onse
amene anali naye anafika olema; ndipo iye anadzitsitsimutsa
kumeneko.

Za uphungu woipa wa Ahiltofeli

15Ndipo Abisalomu, ndi anthu onse amuna a Israyeli, anafika ku
Yerusalemu, ndi Ahitofeli pamodzi naye. 16Ndipo kunali pakudza
kwa Abisalomu Husai M-ariki, bwenzi la Davide, Husai ananena ndi
Abisalomu, Mfumu ikhale ndi moyo, Mfumu ikhale ndi
moyo. 17Ndipo Abisalomu ananena ndi Husai, Kodi cimeneci ndi
cifundo cako ca pa bwenzi lako? unalekeranji kupita ndi bwenzi
lako? 18Husai nanena ndi Abisalomu, lai; koma amene Yehova
anasankha ndi anthu awa, ndi anthu onse a Israyeli, ine ndiri wace,
ndipo ndidzakhala naye iyeyu. 19Ndiponso ndidzatumikira yani? si
pamaso pa mwana wace nanga? monga ndinatumikira pamaso pa
atate wanu, momwemo ndidzakhala pamaso panu, 20Pomwepo
Abisalomu ananena ndi Ahitofeli, Upangire cimene ukuti
rikacite. 21Ndipo Ahitofeli ananena ndi Abisalomu, Mulowe kwa
akazi ang'ono a atate wanu amene iye anawasiya kuti asunge
nyumbayo; ndipo Aisrayeli onse adzamva kuti atate wanu aipidwa
nanu; pomwepo manja a onse akukhala nanu
adzalimba. 22Comweco iwo anayalira Abisalomu hema pamwamba
pa nyumba; ndipo Abisalomu analowa kwa akazi ang'ono a atate
wace pamaso pa Aisrayeli onse. 23Ndipo uphungu wa Ahitofeli
anaupangira masiku aja, unali monga ngati munthu anafunsira
mau kwa Mulungu; uphungu wonse wa Ahitofeli unali wotere kwa
Davide ndi kwa Abisalomu yemwe.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Ndipo Ahitofeli ananena ndi

1Abisalomu, Ndiloleni ndisankhe tsopano anthu zikwi khumi ndi ziwiri, ndipo
ndidzanyamuka usiku womwe uno ndi kulondola Davide; 2ndipo
ndidzamgwera ali wolema ndi wofoka, ndi kumuopsa; ndi anthu onse amene
ali naye adzathawa; pamenepo ndidzakantha mfumu yokha; 3ndipo anthu
onsewo ndidzabwera nao kwa inu; munthu mumfunayo ali ngati onse
obwerera; momwemo anthu onse adzakhala mumtendere. 4Ndipo mauwa
anamuyenerera Abisalomu, ndi akuru onse a Israyeli.

Uphangu wa Husai

5Pomwepo Abisalomu anati, Kaitane tsopano Husai M-ariki yemwe, timvenso
cimene anene iye. 6Ndipo pakufika Husai kwa Abisalomu, Abisalomuyo
ananena naye, Ahitofeli analankhula mau akuti; ticite kodi monga mwa
kunena kwace? ngati iai, unene ndiwe. 7Ndipo Husai ananena ndi Abisalomu,
Uphungu anaupangira lero Ahitofeli suli wabwino. 8Husai anatinso, Mudziwa
atate wanu ndi anthu ace kuti ndizo ngwazi, ndipo ali ndi mitima yowawa
monga cimbalangondo cocilanda ana ace kuthengo; ndipo atate wanu ali
munthu wodziwa nkhondo, sadzagona pamodzi ndi anthu. 9Onani, tsopanoli
alikubisala kudzenje kapena kwina; ndipo kudzali poyamba kugwa ena, ali
yense wakumva adzanena, Alikuphedwa anthu otsata Abisalomu. 10Ndipo
ngakhale ngwazi imene mtima wace ukunga mtima wa mkango
idzasungunuka konse, pakuti Aisrayeli onse adziwa atate wanu kuti ndiye
munthu wamphamvu, ndi iwo ali naye ndiwo ngwazi. 11Koma uphungu wanga
ndiwo kuti musonkhanitse Aisrayeli onse kwa inu kuyambira ku Dani kufikira
ku Beereseba, monga mcenga uli panyanja kucuruka kwao; ndi kuti muturuke
kunkhondo mwini wace. 12Comweco tidambvumbulukira pa malo akuti
adzapezeka, ndipo tidzamgwera monga mame agwa panthaka, ndipo
sitidzasiya ndi mmodzi yense wa iye ndi anthu onse ali naye. 13Ndiponso
ngati walowa ku mudzi wina, Aisrayeli onse adzabwera ndi zingwe kumudziko,
ndipo tidzaukokera kumtsinje, kufikira sikapezeka kamwala kakang'ono
kumeneko. 14Ndipo Abisalomu ndi anthu onse a Israyeli anati, Uphungu wa
Husai M-ariki uposa uphungu wa Ahitofeli. Pakuti kunaikidwa ndi Yehova
kutsutsa uphungu wabwino wa Ahitofeli kuti Yehova akamtengere
Abisalomucoipa.

15Pomwepo Husai ananena ndi Zadoki ndi Abyatara ansembewo, Ahitofeli
anapangira Abisalomu ndi akuru a Israyeli zakuti zakuti; koma ine
ndinapangira zakuti zakuti. 16Cifukwa cace tsono mutumize msanga nimuuze
Davide kuti, Musagona usiku uno pa madooko a kucipululu, koma muoloke
ndithu, kuti mfumu ingamezedwe ndi anthu onse amene ali naye. 17Ndipo
Jonatani ndi Ahimaazi anakhala ku Enirogeli; mdzakazi adafopita kuwauza;
ndipo iwo anapita nauza mfumu Davide, pakuti sangaoneke iwowo alikulowa
m'mudzi. 18Koma mnyamata wina anawaona nauza Abisalomu; ndipo ajawo
anacoka msanga onse awiri, nafika ku nyumba ya munthu ku Bahurimu,
amene anali naco citsime pabwalo pace; ndipo anatsikira m'menemo. 19Ndipo
mkazi anatenga cibvundikilo naciika pakamwa pa citsime, napapasapo
lipande la tirigu; momwemo sicinadziwika. 20Ndipo anyamata a Abisalomu
anafika kunyumba kwa mkaziyo; nati, Ali kuti Ahimaazi ndi Jonatani? Ndipo
mkaziyo ananena nao, Anaoloka kamtsinje kamadzi. Ndipo atawafunafuna,
osawapeza, anabwerera kumka ku Yerusalemu.

Davide ndi anthu ace aoloka Yordano

21Ndipo kunali, atapita iwo, ajawo anaturuka m'citsime, namka nauza mfumu
Davide; nati kwa Davide, Nyamukani nimuoloke madzi msanga; pakuti

Ahitofeli anapangira zotere pa inu. 22Pomwepo Davide ananyamuka ndi anthu
onse amene anali naye, naoloka Yordano. Kutaca m'mawa sanasowa mmodzi
wa iwo wosaoloka Yordano. 23Ndipo Ahitofeli, pakuona kuti sautsata uphungu
wace anamanga buru wace, nanyamuka, nanka kumudzi kwao, nakonza za pa
banja lace, nadzipacika, nafa, naikidwa m'manda a atate wace.

Abisalomu ndi anthu ace aolokanso Yordano

24Ndipo Davide anafika ku Mahanaimu. Abisalomu naoloka Yordano, iye ndi
anthu onse a Israyeli pamodzi naye. 25Ndipo Abisalomu anaika Amasa,
kazembe wa khamulo, m'malo a Yoabu. Koma Amasayu ndiye mwana wa
munthu dzina lace Itra M-israyeli, amene analowa kwa Abigayeli, mwana
wamkazi wa Nahasi, mlongo wa Zeruya, amai a Yoabu. 26Ndipo Israyeli ndi
Abisalomu anamanga zithando m'dziko la Gileadi.

Nkhondo imlaka Abisalomu, naphedwa iye mwini

27Ndipo kunali pakufika Davide ku Mahanaimu, Sobi mwana wa Nahasi wa ku
Raba wa ana a Amoni, ndi Makiri mwana wa Amiyeli wa ku Lodebara, ndi
Barizilai Mgileadi wa ku Rogelimu, 28iwo anabwera nao makama, ndi mbale,
ndi zotengera zadothi, ndi tirigu, ndi barele, ndi ufa, ndi tirigu wokazinga, ndi
nyemba, ndi mphodza, ndi zokazinga zina, 29ndi uci ndi mafuta, ndi nkhosa,
ndi mase a ng'ombe, kutiadye Davide, ndi anthu amene anali naye; pakuti
anati, Anthu ali ndi njala, olema, ndi aludzu m'cipululumo.

1Ndipo Davide anawerenga anthu amene anali naye, nawaikira
atsogoleri a zikwi ndi atsogoleri a mazana. 2Davide natumiza anthu
atawagawa magulu atatu, gulu limodzi aliyang'anire Yoabu, lina
aliyang'anire Abisai, mwana wa Zeruya, mbale wa Yoabu, ndi lina
aliyang'anire Itai Mgiti. Ndipo mfumu inanena ndi anthu, Zoonadi
ine ndemwe ndidzaturuka limodzi ndi inu. 3Koma anthuwo anati,
Simudzaturuka ndinu; pakuti tikathawa sadzatisamalira ife;
ngakhale limodzi la magawo awiri a ife likafa sadzatisamalira; koma
inu mulingana ndi zikwi khumi a ife; cifukwa cace tsono nkwabwino
kuti mutithandize kuturuka m'mudzi. 4Ndipo mfumu inanena nao,
Ndidzacita cimene cikomera inu. Mfumu niima pambali pa cipata,
ndipo anthu onse anaturuka ali mazana, ndi zikwi. 5Ndipo mfumu
inalamulira Yoabu nd Abisai ndi Itai, kuti, Cifukwa ca ine mucite
mofatsa ndi mnyamatayo, Abisalomu. Ndipo anthu onse anamva
pamene mfumu inalamulira atsogoleriwo za Abisalomu. 6Comweco
anthuwo anaturukira kuthengo kukamenyana ndi Israyeli;
nalimbana ku nkhalango ya ku Efraimu. 7Ndipo anthu a Israyeli
anakanthidwa pamenepo pamaso pa anyamata a Davide, ndipo
kunali kuwapha kwakukuru kumeneko tsiku lomwelo, anthu zikwi
makumi awiri. 8Pakuti nkhondo inatanda pa dziko lonse, ndipo tsiku
lomwelo nkhalango inaononga anthu akuposa amene anaonongeka
ndi lupanga. 9Ndipo Abisalomu anakomana ndi anyamata a Davide.
Abisalomu naberekeka pa nyuru yace, ndipo nyuruyo inapita pansi
pa nthambi zolimba za thundu wamkuru. Ndipo mutu wace
unakodwa ndi mtengo, iye ali lende pakati pa thambo ndi pansi ndi
nyuru imene inali pansi pa iye Inapitirira. 10Ndipo munthu wina
anamuona, nauza Yoabu, nati, Onani, ndaona Abisalomu ali lende
pathundu. 11Ndipo Yoabu ananena ndi womuuzayo, Ndipo taona,
unamuona, tsono unalekeranji kumkantha agwe pansi pomwepo?
ndipo ine ndikadakupatsa ndarama khumi ndi lamba. 12Munthuyo
nanena ndi Yoabu, Ndingakhale ndikalandira ndarama cikwi
m'dzanja langa, koma sindikadasamula dzanja langa pa mwana wa
mfumu; pakuti m'kumva kwathu mfumu inalamulira inu ndi Abisai
ndi Itai, kuti, Cenjerani munthu yense asakhudze mnyamatayo
Abisalomu. 13Ndikadacita conyenga pa moyo wace, palibe mrandu
ubisika kwa mfumu; ndipo inu nomwe mukadanditsuta. 14Pomwepo
Yoabu anati, Sindiyenera kucedwa nawe. Natenga mikondo itatu
nagwaza nayo mtima wa Abisalomu alikukhala wamoyo pakati pa
mtengowo. 15Ndipo anyamata khumi onyamula zida zace za Yoabu
anamzungulira Abisalomu namkantha namupha. 16Ndipo Yoabu
analiza lipenga, ndipo anthu anabwerera naleka kupitikitsa
Aisrayeli; pakuti Yoahu analetsa anthuwo. 17Ndipo anatenga
Abisalomu namponya m'cidzenje cacikuru kunkhalangoko; naunjika

pamwamba pace mulu waukuru ndithu wamiyala; ndipo Aisrayeli onse anathawa yense ku hema wace. 18Koma Abisalomu akali moyo adatenga nadziutsira coimiritsaco ciri m'cigwa ca mfumu; pakuti anati, Ndiribe mwana wamwamuna adzakhala cikumbutso ca dzina langa; nacha coimiritsaco ndi dzina la iye yekha; ndipo cichedwa cikumbutso ca Abisalomu, kufikira lero lomwe.

Davide alira Abisalomu

19Pomwepo Ahimaazi mwana wa Zadoki anati, Ndithamange nditengere mfumu mau kuti Yehova wabwezera cilango adani ace. 20Ndipo Yoabu ananena naye, Sudzakhala iwe wotengera mau lero, koma tsiku lina udzatengera mau; koma lero sudzatengera mau, cifukwa mwana wa mfumu wafa. 21Pamenepo Yoabu ananena ndi Mkusi, Kauze mfumu zimene unaziona. Ndipo Mkusi anawerama kwa Yoabu, nathamanga. 22Ndipo Ahimaazi mwana wa Zadoki ananena kaciwiri kwa Yoabu, Komatu, mundilole ndithamange inenso kutsata Mkusi. Ndipo Yoabu anati, Udzathamangiranji, mwana wanga, popeza sudzalandira mphotho ya pa mauwo? 23Koma ngakhale kotero, anati iye, Ndithamange, iye nanena naye, Thamanga. Ndipo Ahimaazi anathamanga njira ya kucigwa, napitirira Mkusi.

24Koma Davide anakhala pakati pa zipata ziwiri; ndipo mlonda anakwera pa tsindwi la cipata ca kulinga, natukula maso ace, napenya; naona munthu alikuthamanga yekha. 25Pamenepo mlondayo anapfuula, nauza mfumu. Mfumuyo niti, Ngati ali yekha alikubwera ndi mau. Ndipo iye uja anayenda msanga, nayandikira. 26Ndipo mlondayo anaona munthu wina wothamanga; mlonda naitana wakucipata nanena, Taona munthu wina wakuthamanga yekha. Ndipo mfumu inati, iyenso abwera ndi mau. 27Mlondayo nati, Ndiyesa kuti kuthamanga kwa wapatsogoloyo kunga kuthamanga kwa Ahimaazi mwana wa Zadoki, Ndipo mfumu inati, iye ndiye munthu wabwino, alikubwera ndi mau okoma. 28Ndipo Ahimaazi anapfuula, nanena ndi mfumu, Mtendere. Ndipo anawerama pamaso pa mfumu ndi nkhope yace pansi, nati, Alemekezeke Yehova Mulungu wanu amene anapereka anthu akukwezera dzanja lao pa mbuye wanga mfumu. 29Ndipo mfumu inati, Kodi mnyamatayo Abisalomu ali bwino? Ahimaazi nayankha, Pamene Yoabu anatumiza mnyamata wa mfumu, ndiye ine mnyamata wanu, ndinaona piringu piringu, koma sindinadziwa ngati kutani. 30Ndipo mfumu inati, Pambuka nuime apa. Napambuka, naimapo. 31Ndipo onani, Mkusiyo anafika, nati, Mau akuuza mbuye wanga mfumu; pakuti Yehova anabwezera cilango lero onse akuukira inu. 32Ndipo mfumu inanena ndi Mkusiyo, Mnyamatayo Abisalomu ali bwino? Mkusiyo nayankha, Adani a mbuye wanga mfumu, ndi onse akuukira inu kukucitirani zoipa,

akhale monga mnyamata ujayo. 33Ndipo mfumuyo inagwidwa cisoni, nikwera ko cipinda cosanja pa cipataco, nilira misozi; niyenda, nitero, Mwana wanga Abisalomu, mwana wanga Abisalomu; mwana wanga! Mwenzi nditakufera ine, Abisalomu, mwana wanga, mwana wanga!

©The Bible Society of Malawi, 1992

Yoabu adzudzula Davide

1Ndipo anauza Yoabu, Onani mfumu irikulira misozi, nilira
Abisalomu. 2Ndipo cipulumutso ca tsiku lila cinasandulika maliro
kwa anthu onse; pakuti anthu anamva kuti, Mfumu iri ndi cisoni
cifukwa ca mwana wace. 3Ndipo tsiku lija anthu analowa m'mudzi
kacetecete, monga azemba anthu akucita manyazi pakuthawa
nkhondo. 4Ndipo mfumu inapfunda nkhope yace, nilira ndi mau
okweza, Mwana wanga Abisalomu, Abisalomu, mwana wanga,
mwana wanga, 5Ndipo Yoabu anafika ku nyumba ya mfumu, nati,
Lero mwacititsa manyazi nkhope zao za anyamata anu onse,
amene anapulumutsa moyo wanu lero, ndi miyoyo ya ana anu
amuna ndi akazi, ndi miyoyo ya akazi anu, ndi miyoyo ya akazi anu
ang'ono; 6m'mene mukonda awo akudana nanu, ndi kudana nao
amene akukondani. Pakuti lero mwalalikira kuti simusamalira konse
akalonga ndi anyamata; pakuti lero ndizindikira kuti tikadafa ife
tonse, ndipo akadakhala ndi moyo Abisalomu, pamenepo
mukadakondwera ndithu. 7Cifukwa cace tsono nyamukani,
muturuke, nimulankhule zowakondweretsa anyamata anu; pakuti
ndilumbira, Pali Yehova, kuti mukapanda kuturuka inu, palibe
munthu mmodzi adzakhala nanu usiku uno; ndipo cimeneci
cidzakuipirani koposa zoipa zonse zinakugwerani kuyambira
ubwana wanu kufikira tsopanoli. 8Pamenepo mfumu inanyamuka,
nikakhala pacipata, Ndipo inauza anthu kuti, Onani mfumu
irikukhala pacipata; anthu onse nadza pamaso pa mfumu. Koma
Aisrayeli adathawa, munthu yense ku hema wace. 9Ndipo anthu
onse a m'mafuko onse a Israyeli analikutsutsana, ndi kuti,
Mfumuyo inatilanditsa ife m'dzanja la adani athu, natipulumutsa
m'dzanja la Afilisti; ndipo tsopano inathawa m'dziko kuthawa
Abisalomu. 10Ndipo Abisalomu amene tinamdzoza mfumu yathu
anafa kunkhondo. Cifukwa cace tsono mulekeranji kunena mau
akuti abwere nayo mfumuyo?

Davide abwerera kumka ku Yerusalemu

11Ndipo mfumu Davide anatumiza kwa Zadoki ndi Abyatara
ansembewo, nati, Mulankhule nao akuru a Yuda, kuti, Mukhale
bwanji am'mbuyo kubwera nayo mfumu ku nyumba yace? pakuti
mau a Aisrayeli onse anafika kwa mfumu akuti abwere nayo ku
nyumba yace. 12Inu ndinu abale anga, muli pfupa langa ndi mnofu
wanga; cifukwa ninji tsono muli am'mbuyo koposa onse kubwera
nayo mfumu? 13Ndipo munene ndi Amasa, Suli pfupa langa ndi
mnofu wanga kodi? Mulungu andilange naonjezepo ngati
sudzakhala cikhalire kazembe wa khamu la ankhondo pamaso
panga, m'malo mwa Yoabu. 14Ndipo iye anakopa mitima ya anthu
onse a Yuda, monga munthu mmodzi, natumiza iwo kwa mfumu,

nati, Mubwere inu ndi anyamata anu onse. 15Comweco mfumu
inabwera nifika ku Yordano. Ndipo Ayuda anadza ku Giligala, kuti
akakomane ndi mfumu, ndi kumuolotsa mfumu pa Yordano.
16Ndipo Simeyi, mwana wa Gera, Mbenjammi, wa ku Bahurimu,
anafulumira natsika pamodzi ndi anthu a Yuda kuti akakomane ndi
mfumu Davide. 17Ndipo anali nao anthu cikwi cimodzi Abenjamini,
ndi Ziba mnyamata wa nyumba ya Saul; ndi ana ace amuna khumi
ndi asanu, ndi anyamata ace makumi awiri pamodzi naye; iwo
naoloka Yordano pamaso pa mfumu. 18Ndipo ngalawa yakuolotsera
inaoloka kuti akatenge banja la mfumu ndi kucita comkomera.
Ndipo Simeyi mwana wa Gera anagwa pansi pamaso pa mfumu
pakuoloka iye pa Yordano. 19Nati kwa mfumu, Mbuye wanga
asandiwerengere ine mphulupulu ndiponso musakumbukile cimene
mnyamata wanu ndinacita mwamphulupulu tsiku lila mbuye
wanga mfumu anaturuka ku Yerusalemu, ngakhale kucisunga
mumtima mfumu. 20Pakuti mnyamata wanu ndidziwa kuti
ndinacimwa; cifukwa cace, onani, ndinadza lero, ndine woyamba
wa nyumba yonse ya Yosefe kutsika kuti ndikomane ndi mbuye
wanga mfumu. 21Koma Abisai mwana wa Zeruya anayankha nati,
Kodi sadzaphedwapo Simeyi cifukwa ca kutemberera wodzozedwa
wa Yehova? 22Koma Davide anati, Ndiri ndi ciani inu, ana a Zeruya
inu, kuti muzikhala akutsutsana ndi ine lero? Kodi munthu
adzaphedwa m'Israyeli lero? Sindidziwa kodi kuti ndine mfumu ya
Israyeli lero? 23Ndipo mfumu inanena ndi Simeyi, Sudzafa. Mfumu
nimlumbirira iye.

Mefiboseti akomana ndi Davide

24Ndipo Mefiboseti mwana wa Sauli anatsika kukakomana ndi
mfumu; ndipo sadasamba mapazi ace, kapena kumeta ndebvu
zace, kapena kutsuka zobvalazace kuyambira tsiku lomuka
mfumukufikira tsiku lobwera kwao mumtendere. 25Ndipo kunali
pakufika iye ku Yerusalemu kukakomana ndi mfumu, mfumu
inanena naye, Cifukwa ninji sunapita nane Mefiboseti? 26Ndipo
anayankha, Mbuye wanga mfumu, mnyamata wanga
anandinyenga; pakuti mnyamata wanu ndinati, Ndidzadzimangira
buru kuti ndiberekekepo ndi kupita ndi mfumu, pakuti mnyamata
wanu ndiri wopunduka. 27Ndipo iye anandinamizira mnyamata
wanu kwa mbuye wanga mfumu; koma mbuye wanga mfumu ali
ngati mthenga wa Yehova; cifukwa cace citani cimene
cikukomerani. 28Pakuti nyumba yonse ya atate wanga inali anthu
oyenera imfa pamaso pa mbuye wanga mfumu; koma inu munaika
mnyamata wanu pakati pa iwo akudya pa gome lanu. Kuyenera
kwanga nkutaninso kuti ndikaonjeze kudandaulira kwa
mfumu? 29Ndipo mfumu inanena naye, Ulikulankhulanso bwanji za
zinthu zako? Ine ndikuti, Iwe ndi Ziba mugawe dzikolo. 30Ndipo

Mefiboseti anati kwa mfumu, Lingakhale lonselo alitenge, popeza mbuye wanga mfumu wabwera mumtendere ku nyumba yace.

Barizilai akomana ndi Davide

31Ndipo Barizilai, Mgileadi anatsika kucokera ku Rogelimu; nayambuka pa Yordano ndi mfumu, kuti akamuolotse pa Yordano. 32Ndipo Barizilai anali nkhalamba, ndiye wa zaka makumi asanu ndi atatu; ndiye amene anapereka cakudya kwa mfumu muja anagona ku Mahanaimu, pakuti anali munthu womveka ndithu. 33Ndipo mfumu inanena ndi Barizilai, Tiyeni muoloke nane, ndipo ndidzakusungani pamodzi ndi ine ku Yerusalemu. 34Koma Barizilai ananena ndi mfumu, Masiku a zaka za moyo wanga ndiwo angati, kuti ndiyenera kukwera ndi mfumu kumka ku Yerusalemu? 35Lero ndiri nazo zaka makumi asanu ndi atatu; kodi ndikhoza kuzindikiranso kusiyanitsa zabwino ndi zoipa? Mnyamata wanu ndikhoza kodi kuzindikira cimene ndidya kapena kumwa? Kodi ndikhozanso kumva mau a amuna ndi akazi oyimba? Cifukwa ninji tsono mnyamata wanu ndidzakhalanso wolemetsa mbuye wanga mfumu. 36Mnyamata wanu angofuna kuoloka Yordano pamodzi ndi mfumu; ndipo afuniranji mfumu kundibwezerapo mphothoyotere? 37Mulole mnyamata wanu ndibwererenso, kuti ndikamwalire m'mudzi wanga ku manda a atate wanga ndi mai wanga. Koma suyu, Cimamu mnyamata wanu, iye aoloke pamodzi ndi mbuye wanga mfumu, ndipo mumcitire cimene cikukomerani. 38Ndipo mfumu inayankha, Cimamu adzaoloka nane, ndipo ndidzamcitira cimene cikukomereni; ndipo ciri conse mukadzapempha kwa ine ndidzakucitirani inu. 39Ndipo anthu onse anaoloka Yordano, ndi mfumu yomwe inaoloka; ndipo mfumuyo Inapsompsona Barizilai nimdalitsa; ndipo iye anabwerera kunka kumalo kwace.

Nsanje pakati pa Yuda ndi Israyeli

40Comweco mfumu inaoloka nifika ku Giligala, ndi Cimamu anaoloka naye, ndipo anthu onse a Yuda adaolotsa mfumu, ndiponso gawo lina la anthu a Israyeli. 41Ndipo onani, Aisrayeli onse anafika kwa mfumu, nanena ndi mfumu, Abale athu anthu a Yuda anakucotsani bwanji mwakuba, naolotsa mfumu ndi banja lace pa Yordano, ndi anthu onse a Davide pamodzi naye? 42Ndipo anthu onse a Yuda anayankha anthu a Israyeli. Cifukwa mfumu iri ya cibale cathu; tsono mulikukwiyiranji pa mrandu umenewu? tinadya konse za mfumu kodi? kapena kodi anatipatsa mtulo uli wonse? 43Ndipo anthu a Israyeli anayankha anthu a Yuda, nati, Ife tiri ndi magawo khumi mwa mfumu, ndi mwa Davide koposa inu; cifukwa ninji tsono munatipeputsa ife, osayamba kupangana nafe za kubwezanso mfumu yathu? Koma mau a anthu a Yuda anali aukali koposa mau a anthu a Israyeli.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Mpanduko ndi imfa ya Seba

1Ndipo kudangotero kuti pamenepo panali munthu woipa, dzina
lace ndiye Seba mwana wa Bikri Mbenjamini; naliza iye lipenga,
nati, Ife tiribe gawo mwa Davide, tiribenso colowa mwa mwana wa
Jese; munthu yense apite ku mahema ace, Israyeli inu. 2Comweco
anthu onse a Israyeli analeka kutsata Davide, natsata Seba mwana
wa Bikri; koma anthu a Yuda anaphatikizana ndi mfumu yao,
kuyambira ku Yordano kufikira ku Yerusalemu.
3Ndipo Davide anafika kunyumba kwace ku Yerusalemu. Mfumuyo
nitenga akazi khumi ang'onowo amene adawasiya asunge
nyumbayo, nawatsekera m'nyumba, nawapatsa cakudya, koma
sanalowana nao. Comweco iwowa anatsekedwa kufikira tsiku la
imfa yao, nakhala ngati akazi amasiye.
4Pamenepo mfumu inati kwa Amasa, Undiitanire anthu a Yuda
asonkhane asanapite masiku atatu, nukhale pano
iwenso. 5Comweco Amasa anamuka kukaitana anthu a Yuda
asonkhane; koma anacedwa, napitiriza nthawi imene
idamuikira. 6Ndipo Davide anati kwa Abisai, Tsopano Seba mwana
wa Bikri adzaticitira coipa coposa cija ca Abisalomu; utenge
anyamata a mbuye wako numtsatire, kuti angapeze midzi ya
malinga ndi kupulumuka osaonekanso. 7Ndipo anaturuka namtsata
anthu a Yoabu, ndi Akereti ndi Apeleti, ndi anthu onseamphamvu;
naturuka m'Yerusalemu kukalondola Seba mwana wa
Bikri. 8Pamene anafika iwo pa mwala waukuru uli ku Gibeoni,
Amasa anadza kukomana nao. Ndipo Yoabu atabvala mwinjiro
wace, anadzimangirira lamba lolongamo lupanga m'cimace
m'cuuno mwace; ndipo m'kuyenda kwace lidasololoka. 9Ndipo
Yoabu ananena ndi Amasa, Uli bwino mbale wanga? Ndipo Yoabu
anagwira ndebvu za Amasa ndi dzanja lace lamanja kuti
ampsompsone. 10Koma Amasa sanasamalira lupanga liri m'dzanja
la Yoabu; comweco iye anamgwaza nalo m'mimba; nakhuthula
matumbo ace pansi, osamgwazanso; nafa iye, Ndipo Yoabu ndi
Abisai mbale wace analondola Seba mwana wa Bikri. 11Ndipo
mnyamata wina wa Yoabu anaima pali iye, nati, Wobvomereza
Yoabu, ndi iye amene ali wace wa Davide, atsate Yoabu. 12Ndipo
Amasa analikukunkhulira m'mwazi wace pakati pa mseu. Ndipo
pamene munthuyo anaona kuti anthu onse anaima, iye
ananyamula Amasa namcotsa pamseu kumka naye kuthengo,
nampfunda ndi cobvala, pamene anaona kuti anaima munthu
yense wakufika pali iye. 13Atamcotsa iye mumseu, anthu onse
anapitirira kumsata Yoabu kukalondola Seba mwana wa
Bikri. 14Ndipo anapyola mapfuko onse a Israyeli kufikira ku Abeli

ndi ku Betimaaka, ndi kwa Aberi onse; iwo nasonkhana pamodzi namlondolanso. 15Ndipo anadza nammangira misasa m'Abeli wa Betimaaka, naundira nthumbira pa mudziwo, ndipo unagunda tioga; ndipo anthu onse akukhala ndi Yoabu anakumba lingalo kuti aligwetse. 16Pamenepo mkazi wanzeru wa m'mudzimo anapfuula, kuti, Imvani, imvani; munene kwa Yoabu, Bwerani pafupi kuno kuti ndgankhule nanu. 17Ndipo anayandikira kwa mkaziyo; ndi mkaziyo anati, Ndinu Yoabu kodi? iye nayankha, Ndine amene. Pamenepo ananena naye, Imvani mau a mdzakazi wanu. Iye nayankha, Ndirikumva. 18Ndipo iye analankhula, nati, Kale adafunena kuti, Zoonadi adzapempha uphungu ku Abeli; ndipo potero mrandu udafukutha. 19Inendine wa awo amene ali amtendere ndi okhulupirika m'Israyeli; inu mulikufuna kuononga mudzi ndi mai wa m'Israyeli; mudzamezerang colowa ca Yehova? 20Ndipo Yoabu anayankha nati, Iai ndi pang'ono ponse, cikhale kutali kwa ine, kuti ndingameze ndi kuononga. 21Mranduwo soli wotere ai, koma munthu wa ku dziko lamapiri la Efraimu, dzina lace ndiye Seba mwana wa Bikri, anakweza dzanja lace pa mfumu Davide; mpereke iye yekha ndipo ndidzacoka kumudzi kuno. Ndipo mkaziyo anati kwa Yoabu, Onani tidzakuponyerani mutu wace kutumphitsa Gnga. 22Pomwepo mkaziyo anapita kwa anthu onse mwa nzeru yace. Ndipo iwo anadula mutu wa Seba mwana wa Bikri, nauponya kunja kwa Yoabu. Ndipo analiza Gpenga, nabalalika kucoka pamudzipo, munthu yense kumka ku hema wace. Ndipo Yoabu anabwerera kumka ku Yerusalemu kwa mfumu.
23Ndipo Yoabu anali woyang'anira khamu lonse la Israyeli; ndi Benaya, mwana wa Jehoyada, anayang'anira Akereti ndi Apeleti; 24ndi Adoramu anayang'anira msonkho; ndi Jehosafati mwana wa Ahiludi anali wolemba mbiri; 25ndi Seva anali mlembi; ndi Zadoki ndi Abyatara anali ansembe; 26ndiponso Ira Mjairi anali nduna ya Davide.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Njala m'dziko, cifukwa cace, matsirizidwe ace

1Ndipo m'masiku a Davide munali odala, zaka zitatu; ndipo Davide
anafunsira kwa Yehova. Ndipo Yehova anati, Ndico cifukwa ca Sauli
ndi nyumba yace yamwazi, popeza iye anawapha Agibeoni. 2Ndipo
mfumu inaitana Agibeoni, ninena nao (koma Agibeoni sanali a ana
a Israyeli, koma a Aamori otsala; ndipo ana a Israyeli
anawalumbirira kwa iwo, koma Sauli anafuna kuwapha mwa cangu
cace ca kwa ana a Israyeli ndi a Yuda). 3Ndipo Davide ananena ndi
Agibeoni, Ndidzakucitirani ciani, ndipo ndidzakuyanjanitsani ndi
ciani kuti mukadalitse colowa ca Yehova? 4Ndipo Agibeoni ananena
naye, Sitifuna siliva kapena golidi wa Sauli kapena nyumba yace;
ndiponso sitifuna kupha munthu ali yense wa m'Israyeli. Nati iye,
Monga inu mudzanena, momwemo ndidzakucitirani. 5Ndipo anati
kwa mfumu, Munthu uja anatitha natilingalira pa ife cotionongera
kuti tisakhalenso m'malire ali onse a Israyeli, 6mutipatse ana ace
amuna asanu ndi awiri, ndipo tidzawapacika kwa Yehova m'Gibeya
wa Sauli, wosankhika wa Yehova, Mfumu niti,
Ndidzawapereka. 7Koma mfumu inaleka Mefiboseti mwana wa
Jonatani, mwana wa Sauli, cifukwa ca lumbiro la kwa Yehova linali
pakati pa Davide ndi Jonatani mwana wa Sauli. 8Koma mfumu
inatenga ana amuna awiri a Rizipa mwana wamkazi wa Aya,
amene anambalira Sauli, ndiwo Arimoni ndi, Mefiboseti; ndiponso
ana amuna asanu a Mikala, mwana wamkazi wa Sauli, amene iye
anambalira Adriyeli mwana wa Barizilai Mmeholati; 9niwapereka
m'manja a Agibeoni, iwo nawapacika m'phiri pamaso pa Yehova,
ndipo anagwa pamodzi onse asanu ndi awiri; m'masiku a kukolola,
m'masiku oyamba, poyamba kuceka barele. 10Ndipo Rizipa mwana
wamkazi wa Aya anatenga ciguduli, nadziyalira ici pathanthwe,
kuyambira pakukolola kufikira madzi ocokera kumwamba
adawagwera; ndipo sadalola mbalame za m'mlengalenga kutera
pa iwo usana, kapena zirombo za kuthengo usiku. 11Ndipo anauza
Davide cimene Rizipa mwana wamkazi wa Aya, mkazi wamng'ono
wa Sauli anacita. 12Ndipo Davide ananka natenga mafupa a Sauli
ndi mafupa a Jonatani mwana wace kwa anthu a ku Jabezi Gileadi
amene anawaba m'khwalala la Betisani, kumene Afilisti
adawapacika, tsiku lija Afilistiwo anapha Sauli ku Giliboa; 13nacotsa
kumeneko mafupa a Sauli ndi mafupa a Jonatani mwana wace;
nasonkhanitsa iwo mafupa a iwo aja adapacikidwa. 14Naika
mafupa a Sauli ndi Jonatani mwana wace ku dziko la Benjamini
m'Zela, m'manda a Kisi atate wace; nacita zonse inalamulira
mfumu. Ndipo pambuyo pace Mulungu anapembedzeka za dzikolo.

Nkhondo zakupha ziphona za Afilisti

15Ndipo Afilisti anaponyananso nkhondo ndi Aisrayeli; ndipo
Davide anatsika ndi anyamata ace pamodzi naye naponyana ndi
Afilisti; nafuna kukomoka Davide. 16Ndipo Isibenobi, ndiye wa ana
a Rafa, amene kulemera kwa mkondo wace kunali masekeli
mazana atatu a mkuwa, iyeyo anabvala lupanga latsopano, nati
aphe Davide. 17Koma Abisai mwana wa Zeruya anamthandiza
namkantha Mfliistiyo, namupha. Pomwepo anthu a Davide
anamlumbirira iye nati, Inu simudzaturuka nafenso kunkhondo,
kuti mungazime nyali ya Israyeli.
18Ndipo kunali citapita ici, kunalinso nkhondo ndi Afilisti ku Gobu;
pamenepo Sibekai Mhusati anapha Safi, ndiye wa ana a
Rafa. 19Ndipo panalinso nkhondo ndi Afilisti ku Gobu; ndipo
Elhanani mwana wa Jare-oregimu wa ku Betelehemu anapha
Goliate Mgiti, amene mtengo wa mkondo wace unanga mtanda wa
woombera nsaru. 20Ndipo panalinso nkhondo ku Gati, kumene
kunali munthu wa msinkhu waukuru, amene anali nazo zala zisanu
ndi cimodzi pa dzanja lonse, ndi pa phazi lonse zala zisanu ndi
cimodzi kuwerenga kwa zonse ndiko makumi awiri ndi zinai; ndipo
iyenso anambala ndi Rafa. 21Ndipo pakutonza Israyeli iyeyu,
Jonatani mwana wa Simeyi mbale wa Davide anamupha. 22Awa
anai anawabala ndi Rafa, ku Gati; ndipo anagwa ndi dzanja la
Davide ndi la anyamata ace.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Nyimbo yoyamikira ya Davide

1Ndipo Davide analankhula kwa Yehova mau a nyimbo iyi tsikuli
Yehova anampulumutsa m'dzanja la adani ace onse, ndi m'dzanja
la Sauli. 2Ndipo anati:-
Yehova ndiye thanthwe langa, ndi ngaka yanga, ndi mpulumutsi
wanga, wangadi;
3Mulungu wa thanthwe langa, Iye ndidzamkhulupirira;
Cikopa canga, ndi nyanga ya cipulumutso canga, nsanja yanga
yaitali, ndi populumukirapo panga;
Mpulumutsi wanga, mundipulumutsa kuciwawa.
4Ndidzaitanakwa Yehovaamene ayenera timtamande;
Comweco ndidzapulumutsidwa kwa adani anga.
5Pakuti mafunde a imfa anandizinga,
Mitsinje ya zopanda pace inandiopsa ine.
6Zingwe za kumanda zinandizingira;
Misampha ya imfa inandifikira ine.
7M'kusauka kwanga ndinaitana kwa Yehova,
Inde ndinakuwira kwa Mulungu wanga;
Ndipo Iye anamva mau anga ali m'kacisi wace,
Ndi kulira kwanga kunafika ku makutuace.
8Pomwepo dziko linagwedezeka ndi kunthunthumira.
Maziko a dziko la kumwamba anasunthika
Nagwedezeka, cifukwa iye anakwiya.
9M'mphuno mwace munaturuka utsi,
Ndi moto woturuka m'kamwa mwace unaononga;
Makala anayaka nao.
10Anaweramitsa miyambanso, natsika;
Ndipo mdima wandiwe-yani unali pansi pa mapazi ace.
11Ndipo iye anaberekeka pa Kerubi nauluka;
Inde anaoneka pa mapiko a mphepo,
12Ndipo anayesa mdimawo ngati mahema omzungulira iye,
Kusonkhana kwa madzi ndi mitambo yocindikira ya mlengalenga.
13Ceza ca pamaso pace
Makala a mota anayaka,
14Yehova anagunda kumwamba;
Ndipo Wam'mwambamwamba ananena mau ace.
15Ndipo iye anatumiza mibvi, nawawaza;
Mphezi, nawaopsa,
16Pamenepo m'munsi mwa nyanja munaoneka,
Maziko a dziko anaonekera poyera,
Ndi mthonzo wa Yehova,
Ndi mpumo wa mweya wa m'mphuno mwace.

17Iye anatumiza kucokera kumwamba nanditenga;
Iye ananditurutsa m'madzi akuru;
18Iye anandipulumutsa kwa mdani wanga wamphamvu,
Kwa iwo akudana ndi ine; pakuti anandiposa mphamvu,
19Anandifikira ine tsiku la tsoka langa;
Koma Yehova anali mcirikizo wanga,
20Iye ananditurutsanso ku malo akuru;
Iye anandipulumutsa, cifukwa akondwera ndi ine.
21Yehova anandibwezera monga mwa colungama canga;
Monga mwa kuvera kwa manja anga anandipatsa mphotho.
22Pakuti ndinasunga njira za Yehova,
Osapambukira koipa kusiya Mulungu wanga.
23Pakuti maweruzo ace onse anali pamaso panga;
Ndipo za malemba ace, sindinawapambukira.
24Ndinakhalanso wangwiro kwa iye,
Ndipo ndinadzisunga kusacita kuipa kwanga.
25Cifukwa cace Yehova anandibwezera monga mwa colungama canga;
Monga mwa kuyera kwanga pamaso pace.
26Ndi acifundo Inu mudzadzionetsa wacifundo,
Ndi munthu wangwiro mudzadzionetsa wangwiro;
27Ndi oyera mtima mudzadzionetsa woyera mtima;
Ndi otsutsatsutsa mudzadzionetsa wopotoza.
28Ndipo mudzapulumutsa anthu osautsidwa;
Koma maso anu ali pa odzikuza kuti muwacepetse.
29Pakuti Inu ndinu nyali yanga, Yehova;
Ndipo Yehova adzaunika mumdima mwanga.
30Pakuti ndi Inu ndithamangira gulu;
Ndi Mulungu wanga ndilumphira linga.
31Kunena za Mulungu, njira yace iri yangwiro;
Mau a Yehova anayesedwa; iye ndiye cikopa kwa onse akukhulupirira iye.
32Pakuti Mulungu ndani, koma Yehova?
Ndipo thanthwe ndani, koma Mulungu wathu?
33Mulungu ndiye Gnga langa lamphamvu;
Ndipo iye ayendetsa angwiro mu njira yace.
34Iye asandutsa mapazi ace akunga mapazi a mbawala;
Nandiika pa misanje yanga.
35Iye aphunzitsa manja anga nkhondo;
Kotero kuti manja anga alifula uta wamkuwa.
36Ndiponso munandipatsa cikopa ca cipulumutso canu;
Ndi kufatsa kwanu kunandikulitsa.
37Munakulitsa kulunza kwanga pansi panga,
Ndi mapazi anga sanaterereka.

38Ndinapitikitsa adani anga, ndi kuwaononga;
Ndiponso sindinabwerera mpaka nditawatha.
39Ndinawatha ndi kuwapyoza, kuti sakhoza kuuka,
Inde anagwa pansi pa mapazi anga.
40Pakuti Inu munandimanga m'cuuno ndi mphamvu ya kunkhondo;
Munandigonjetsera akundiukira.
41Munatembenuzitsanso adani anga andipatse mbuyo,
Kuti ndiwalikhe akudana ndi ine.
42Anayang'ana iwo, koma panalibe wopulumutsa;
Ngakhale kwa Yehova, koma iye sanawayankha.
43Pomwepo ndinawasansantha asalale ngati pfumbi la padziko,
Ndinawapondereza ngati dothi la m'makwalala.
44Inunso munandipulumutsa ine pa kulimbana kwa anthu anga;
Munandisunga ndikhale mutu wa amitundu;
Anthu amene sindinawadziwa adzanditsumikira ine.
45Alendo adzandigonjera ine,
Pakumva za ine, adzandimbera pomwepo.
46Alendo adzafota,
Nadzabwera ndi kunthunthumira oturuka mokwiririka mwao.
47Yehova ali ndi moyo; ndipo lidalitsike thanthwe langa;
Ndipo akulitsidwe Mulungu wa thanthwe la cipulumutso canga;
48Inde Mulungu wakundibwezera cilango ine,
Ndi kundigonjetsera anthu a mitundu.
49Amene anditurutsa kwa adani anga;
Inde mundikweza ine pamwamba pa iwo akundiukira;
Mundipulumutsa kwa munthu waciwawa.
50Cifukwa cace ndidzakuongani Yehova, pakati pa amitundu,
Ndipo ndidzayimba zolemekeza dzina lanu.
51Iye apatsa mfumu yace cipulumutso cacikuru;
Naonetsera cifundo wodzozedwa wace,
Kwa Davide ndi mbeu yace ku nthawi zonse.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Nyimbo yotsiriza ya Davide

1Ndipo mau otsiriza a Davide ndi awa:—
Atero Davide mwana wa Jese,
Atero munthu wokwezedwa,
Ndiye wodzozedwa wa Mulungu wa Yakobo,
Ndi mwini masalmo wokoma wa Israyeli:
2Mzimu wa Yehova unalankhula mwa ine,
Ndi mau ace anali pa lilime langa,
3Mulungu wa Israyeli anati,
Thanthwe la Israyeli Gnalankhula ndi ine;
Kudzakhala woweruza anthu molungama;
Woweruza m'kuopa Mulungu.
4Iye adzakhala ngati kuunika kwa m'mawa, poturuka dzuwa,
M'mawa mopanda mitambo;
Pamene msipu uphuka kuturuka pansi,
Cifukwa ca kuwala koyera, italeka mvula.
5Zoonadi nyumba yanga siikhala yotere ndi Mulungu;
Koma iye anapangana ndi ine pangano losatha,
Lolongosoka mwa zonse ndi losungika;
Pakuti ici ndi cipulumutso canga conse, ndi kufuma kwanga konse,
Kodi sadzacimeretsa?
6Koma oipa onse adzakhala ngati minga yoyenera kuitaya,
Pakuti siigwiridwa ndi dzanja;
7Koma wakukhudza iyo adzikonzeratu citsulo ndi luti la mkondo;
Ndipo idzatenthedwa konse ndi mota m'malo mwao.

Angwazi a Davide

8Maina a ngwazi Davide anali nazo ndiwo: Josebu-basebete Mtakemoni, mkuru wa akazembe; ameneyu ndiye Adino M-ezni wolimbana ndi mazana atatu ophedwa nthawi imodzi. 9Ndipo wotsatana naye Eleazeri mwana wa Dodai mwana wa M-akohi, mmodzi wa ngwazi zitatu zokhala ndi Davide pamene iwo anatonza Afilisti osonkhanidwa kunkhondo kumeneko, atacoka Aisrayeli; 10iye ananyamuka, nakantha Afilisti kufikira dzanja lace linalema, ndi dzanja lace lomamatika kulupanga; ndipo Yehova anacititsa cipulumutso cacikuru tsiku lija, ndipo anthu anabwera m'mbuyo mwace kukafunkha kokha. 11Ndipo wotsatana naye ndiye Sama mwana wa Age Mharario Ndipo Afilisti anasonkhana ali gulu pamene panali munda wamphodza; anthu nathawa Afilistiwo. 12Koma iyeyoanaima pakati pa mundawo, naucinjiriza, napha Afilistiwo. Ndipo Yehova anacititsa cipulumutso cacikuru. 13Ndipo atatu a mwamakumi atatu opambanawo, anatsika nafika kwa Davide nyengo ya kukolola m'phanga la ku

Adulamu; ndi gulu la Afilisti Gnamanga zithando m'cigwa ca Refaimu. 14Pamenepo Davide anali m'linga, ndi boma la Afilisti linali m'Betelehemu. 15Ndipo Davide analakalaka nati, Ha! wina akadandipatsa madzi a m'citsime ca ku Betelehemu ciri pacipatapo! 16Ndipongwazi zitatuzo zinapyola khamu la Afilisti, nizitunga madzi m'citsime ca ku Betelehemu, ca pa cipataco, nawatenga, nafika nao kwa Davide; koma iye sanafuna kumwako, koma anawathira pansi kwa Yehova. 17Nati, Ndisacite ici ndi pang'ono ponse, Yehova; ndimwe kodi mwazi wa anthu awa ana pitawa ndi kutaya moyo wao? Cifukwa cace iye anakana kumwa. Izi anazicita ngwazi zitatuzi. 18Ndipo Abisai, mbale wa Yoabu, mwana wa Zeruya, anali wamkuru wa atatuwa. Iye natukula mkondo wace pa anthu mazana atatu nawapha, natenga dzina iye mwa atatuwa. 19Kodi iye sindiye waulemu mwa atatuwa? cifukwa cace anali kazembe wao; ngakhale iyenso sadafikana ndi atatu oyamba. 20Ndipo Benaya, mwana wa Yehoyada, mwana wa ngwazi wa ku Kabzeli amene anacita zamphamvu; iye anapha anthu awiri a Moabu akunga mikango, natsikanso iye napha mkango m'mbuna nyengo ya cipale cofewa; 21ndipo anapha M-aigupto munthu wokongola, M-aigupto anali nao mkondo m'dzanja lace; koma iyeyo anatsikira kwa iye ndi ndodo, nasolola mkondowo m'dzanja la M-aigupto, namupha ndi mkondo wa iye mwini. 22Izi anacita Benaya mwana wa Yehoyada, natenga dzina mwa ngwazi zitatuzo. 23Iye ndiye waulemu koposa makumi atatuwo, koma sadafikana ndi atatu oyamba. Ndipo Davide anamuika kuyang'anira olindirira ace.
24Asaheli mbale wa Yoabu anali wa makumi atatuwo; Elihanani mwana wa Dodo wa ku Betelehemu; 25Sama Mharodi, Elika Mharodi; 26Helezi Mpaliti, Ira mwana wa Ikesi Mtekoi. 27Abiyezeri M-anetori, Mebunai Mhusati; 28Zalimoni M-ahohi, Maharai Mnefati; 29Helebi mwana wa Baana Mnetofati, ltai mwana wa Ribai wa ku Gibeya wa ana a Benjamini; 30Benaya Mpiratoni, Hidai wa ku timitsinje ta Gaasi; 31Abialiboni M-aribati, Azmaveti Mbahurimi; 32Eliaba Mshaliboni wa ana a Jaseni, Jonatani; 33Sama Mharari, Ahiamu mwana wa Sarari Mharari; 34Elifaleti mwana wa Ahasibai, mwana wa Mmaacha, Eliamu mwana wa Ahitofeli Mgiloni; 35Hezra wa ku Karimeli, Paarai M-aribi; 36Igali mwana wa Natani wa ku Zoba, Bani Mgadi; 37Zeleki M-amoni, Naharai Mbeeroti, onyamula zida za Yoabu mwana wa Zeruya; 38Ira M-itri, Garebi M-itri; 39Uriya Mhiti; onse pamodzi anali makumi atatu mphambu asanu ndi awiri.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Kuwerengedwa kwa anthu kuwatengera cilango ca Mulungu

1Ndipo mkwiyo wa Yehova unayakanso pa Israyeli, nafulumiza
Davide pa iwo, nati, Muka, nuwerenge Israyeli ndi Yuda. 2Ndipo
mfumu inanena ndi Yoabu kazembe wa khamu, amene anali naye,
Kayendere tsopano mafuko onse a Israyeli, kuyambira ku Dani
kufikira ku Beereseba, nuwerenge anthuwo, kuti ndidziwe kucuruka
kwao kwa anthu. 3Ndipo Yoabu ananena ndi mfumu, Yehova
Mulungu wanu aonjezere kwa anthu monga ali kuwacurukitsa
makumi khumi, ndi maso a mbuye wanga mfumu acione; koma
mbuye wanga mfumu alikukondwera bwanji ndi cinthu ici? 4Koma
mau a mfumu anapambana Yoabu ndi atsogoleri a khamulo. Ndipo
Yoabu ndi atsogoleri a khamulo anaturuka pamaso pa mfumu kuti
akawerenge anthu a Israyeli. 5Naoloka Yordano, namanga zithando
ku Aroeri ku dzanja lamanja kwa mudzi uli pakati pa cigwa ca Gadi,
ndi ku Jazeri; 6nafika ku Gileadi ndi ku dera la Tatimuhodisi; nafika
ku Dani-Jaana ndi kuzungulira, kufikira ku Zidoni, 7nafika ku linga la
Turo ndi ku midzi yonse ya Ahivi ndi ya Akanani; naturukira
kumwera kwa Yuda ku Beereseba. 8Comweco pamene atayenda
dziko lonse anafika ku Yerusalemu pakutha miyezi isanu ndi inai,
ndi masiku makumi awiri. 9Ndipo Yoabu anapereka kwa mfumu
kucuruka kwa anthu adawawerenga; ndipo m'Israyeli munali anthu
zikwi mazana asanu ndi atatu, ngwazi zosolola lupanga; ndi anthu
a Yuda ndiwo zikwi mazana asanu.
10Pamenepo mtima wa Davide unamtsutsa, atatha kuwerenga
anthuwoo Davide nati kwa Yehova, Ndinacimwa kwakukuru ndi
cinthu cimene ndinacita; koma tsopano Yehova mucotse
mphulupulu ya mnyamata wanu, pakuti ndinacita kopusa
ndithu. 11Ndipo pouka Davide m'mawa mau a Yehova anafika kwa
mneneri Gadi, mlauli wa Davide, kuti, 12Kalankhule ndi Davide,
Atero Yehova, kuti, Ndikuikira zinthu zitatu; udzisankhire wekha
cimodzi ca izo, ndikakucitire cimeneco. 13Comweco Gadi anafika
kwa Davide, namuuza, nanena naye, Kodi zikugwereni m'dziko
mwanu zaka zisanu ndi ziwiri za njala? Kapena muthawe adani anu
akukupitikitsani miyezi itatu? kapena m'dziko mwanu mukhale
mliri masiku atatu? Cenjerani tsono ndi kulingalira bwino mau
amene ine ndibwere nao kwa wondimumayo. 14Ndipo Davide
ananena ndi Gadi, Ndipsinjika mtima kwambiri, tigwe m'dzanja la
Yehova; pakuti zifundo zace nzazikuru; koma tisagwe m'dzanja la
munthu. 15Comweco Yehova anatumiza mliri pa Israyeli kuyambira
m'mawa kufikira nthawi yoikika; ndipo anafapo anthu zikwi
makumi asanu ndi awiri kuyambira ku Dani kufikira ku
Beereseba. 16Ndipo pamene mthenga anatambasulira dzanja lace

ku Yerusalemu kuuononga, coipaco cinacititsa Yehova cisoni, iye nauza mthenga wakuononga anthuwo, kuti, Kwafikira tsopano, bweza dzanja lako. Ndipo mthenga wa Yehova anali pa dwale la Arauna Mjebusi. 17Ndipo Davide analankhula ndi Yehova pamene anaona mthenga wakudwalitsa anthu, nati, Onani ndacimwa ine, ndinacita mwamphulupulu; koma nkhosa izi zinacitanji? dzanja lanu likhale pa ine ndi pa nyumba ya atate wanga.

Davide ammangira Yehova guwa la nsembe pa dwale la Arauna

18Ndipo Gadi anafika tsiku lomwelo kwa Davide nanena naye, Kwerani mukamangire Yehova guwa la nsembe pa dwale la Arauna Mjebusi. 19Ndipo Davide anakwerako monga mwa kunena kwa Gadi, monga adalamulira Yehova. 20Ndipo Arauna anayang'ana naona mfumuyo ndi anyamata ace alikubwera kwa iye; naturuka Arauna naweramira pamaso pa mfumu nkhope yace pansi. 21Arauna nati, Mbuye wanga mfumu, mwadzeranji kwa mnyamata wanu? Ndipo Davide anati, Kugula dwale lako gi, kuti ndimangirepo Yehova guwa lansembe, kuti mliriwo ulekeke kwa anthu. 22Arauna nati kwa Davide, Mbuye wanga mfumu atenge napereke nsembe comkomera; sizi ng'ombe za nsembe yopsereza, ndi zipangizo ndi zomangira ng'ombe zikhale nkhuni; 23zonsezi, mfumu, Arauna akupatsani mfumu. Ndipo Arauna anati kwa mfumu, Yehova Mulungu wanu akulandireni. 24Koma mfumu inati kwa Arauna, lai; koma ndidzaligula kwa iwe pa mtengo wace, pakuti sindidzapereka kwa Yehova Mulungu wanga nsembe zopsereza zopanda mtengo wace. Momwemo Davide anagula dwalelo ndi ng'ombezo naperekapo masekeli makumi asanu a siliva. 25Ndipo Davide anamangirapo Yehova guwa la nsembe, napereka nsembe zopsereza, ndi nsembe zoyamika. Momwemo Yehova anapembedzeka cifukwa ca dziko, ndi mliri wa pa Israyeli unalekeka.

©The Bible Society of Malawi, 1992

1 Kings

1 Mafuma 1

Ukalamba wa Davide, achula Saloma wodzalowa m'malo mwace

1NDIPO mfumu Davide anakalamba nacuruka masiku ace; ndipo
iwo anampfunda ndi zopfunda, koma iye
sanafundidwa. 2Pamenepo anyamata ace ananena naye, Amfunire
mbuye wanga mfumu namwali, aimirire pamaso pa mfumu
namsunge; nagone m'mfukato mwanu, kuti mbuye mfumu yanga
afundidwe. 3Tsono anafunafuna m'malire monse a Israyeli namwali
wokongola, napeza Abisagi wa ku-Sunamu, nabwera naye kwa
mfumu. 4Ndipo namwaliyo anali wokongola ndithu, namasunga
mfumu namtumikira; koma mfumu sinamdziwa. 5Pamenepo
Adoniya mwana wa Hagiti anadzikuza, nati, Ndikhala mfumu ndine;
nadzikonzera agareta ndi apakavalo ndi anthu makumi asanu
omtsogolera mothamanga. 6Ndipo atate wace sadambvuta masiku
ace onse, ndi kuti, Wlitero cifukwa ninji? Ndiponso anali munthu
wokongola ndithu; napondana ndi Abisalomu. 7Ndipo anapangana
ndi Yoabu mwana wa Zeruya, ndi Abyatara wansembeyo; ndipo
amenewo anamtsata Adoniya namthandiza. 8Koma Zadoki
wansembe, ndi Benaya mwana wace wa Yehoyada, ndi Natani
mneneri, ndi Simeyi, ndi Reyi, ndi anthu amphamvu aja adali ndi
Davide, sanali ndi Adoniya. 9Ndipo Adoniya anapha nkhosa ndi
ng'ombe ndi nyama zonona pamwala pa Zoheleti, uli pafupi ndi
citsime ca Rogeli, naitana abale ace onse ana a mfumu, ndi anthu
onse a Yuda anayamata a mfumu; 10koma Natani mneneriyo, ndi
Benaya, ndi anthu amphamvu aja, ndi Solomo mbale wace,
sanawaitana. 11Pamenepo Natani ananena ndi Batiseba amace wa
Solomo, nati, Kodi sunamva kuti Adoniya mwana wa Hagiti walowa
ufumu, ndipo Davide mbuye wathu sadziwa? 12Ubwere tsono,
ndikupangire, kuti usunge moyo wako, ndi moyo wa mwana wako
Solomo. 13Muka nulowe kwa mfumu Davide, nukati kwa iye, Mbuye
wanga mfumu, kodi simunalumbirira mdzakazi wanu, ndi kuti, Zedi
Solomo mwana wako adzakhala mfumu nditamuka ine, nadzakhala
pa mpando wanga wadfumu? ndipo Adoniya akhaliranji
mfumu? 14Taona, uli cilankhulire ndi mfumu, inenso ndidzalowa
pambuyo pako, ndi kutsimikiza mau ako. 15Pamenepo Batiseba
analowa kwa mfumu kucipinda; ndipo mfumuyo inali yokalamba
ndithu; ndipo Abisagi wa ku Sunamu anali kutumikira
mfumu. 16Ndipo Batiseba anawerama nalambira mfumu, ndi
mfumu niti, Ufunanji? 17Ndipo iye ananena nayo, Mbuye wanga,
munalumbirira mdzakazi wanu pa Yehova Mulungu wanu, ndi kuti,
Zedi Solomo mwana wako adzakhala mfumu nditamuka ine,

nadzakhala pa mpando wanga wacifumu. 18Ndipo tsopano taonani, Adoniva walowa ufumu, ndipo inu mbuye wanga mfumu simudziwa. 19Ndipo iye anapha ng'ombe ndi nyama zonona ndi nkhosa zaunyinji, naitana ana amuna onse a mfumu, ndi Abyatara wansembe, ndi Yoabu kazembe wa nkhondo; koma Solomo mnyamata wanu sanamuitana. 20Ndipo tsopano, mbuye wanga mfumu, maso a Aisrayeli onse ali pa inu, kuti muwauze amene adzakhala pa mpando wacifumu wa mbuye wanga mfumu atamuka iye, 21Mukapanda kutero, kudzacitika, pamene mbuye wanga mfumu atagona kwa makolo ace, ine ndi mwana wanga Solomo tidzayesedwa ocimwa. 22Ndipo taona, iye ali cilankhulire ndi mfumu, Natani mneneriyo analowamo. 23Ndipo anauza mfumu, kuti, Wafika Natani mneneriyo. Ndipo iye anafika pamaso pa mfumu, naweramitsa nkhope yace pansi pamaso pa mfumu. 24Ndipo Natani anati, Mbuye wanga mfumu, kodi inu munati, Adoniya adzakhala mfumu nditamuka ine, nadzakhala ndiye pa mpando wanga wacifumu? 25Popeza iye watsika lero, nakapha ng'ombe ndi nyama zonona ndi nkhosa zaunyinji, naitana ana amuna onse a mfumu, ndi akazembe a nkhondo, ndi Abyatara wansembe; ndipo taonani, iwowo akudya ndi kumwa pamaso pace, nati, Akhale ndi moyo mfumu Adoniya. 26Koma ine, inde inedi mnyamata wanu, ndi Zadoki wansembe, ndi Benaya mwana wa Yehoyada, ndi Solomo mnyamata wanu, sanatiitana. 27Cinthu ici cacitika ndi mbuye wanga mfumu kodi, ndipo simunadziwitsa mnyamata wanu amene adzakhala pa mpando wacifumu wa mbuye wanga mfumu atamuka iye? 28Tsono mfumu Davide anayankha, nati, Ndiitanireni Batiseba. Ndipo iye analowa pamaso pa mfumu, naima pamaso pa mfumu. 29Ndipo mfumu inalumbira, niti, Pali Yehova amene anapulumutsa moyo wanga m'nsautso monse, 30zedi monga umo ndinalumbirira iwe pa Yehova Mulungu wa Israyeli, ndi kuti, Zoonadi Solomo mwana wako adzakhala mfumu nditamuka ine, nadzakhala pa mpando wanga wacifumu m'malo mwa ine, zedi nditero lero lomwe. 31Pamenepo Batiseba anaweramitsa pansi nkhope yace, nalambira mfumu, nati, Mbuye wanga mfumuakhale ndi moyo nthawi zamuyaya. 32Ndipo mfumu Davide anati, Kandiitanireni Zadoki wansembeyo, ndi Natani mneneriyo, ndi Benaya mwana wa Yehoyada. Iwo nalowa pamaso pa mfumu. 33Ndipo mfumu inati kwa iwo, Tengani akapolo a mfumu yanu, nimukweze Solomo mwana wanga pa nyuru yanga yanga, nimutsikire naye ku Gihoni. 34Ndipo Zadoki wansembe ndi Natani mneneri akamdzoze kumeneko akhale mfumu ya Israyeli; ndipo muombe lipenga, ndi kuti, Mfumu Solomo akhale ndi moyo. 35Pamenepo mumtsate iye, iye nadzadza nadzakhala pa mpando wanga wacifumu, popeza adzakhala iyeyu mfumu m'malo

mwanga; ndipo ndamuika iye akhale mtsogoleri wa lsrayeli ndi Yuda. 36Ndipo Benaya mwana wa Yehoyada anayankha mfumu, nati, Amen, ateronso Yehova Mulungu wa mbuye wanga mfumu. 37Monga umo Yehova anakhalira ndi mbuye wanga mfumu, momwemo akhalenso ndi Solomo, nakuze mpando wace wacifumu upose mpando wacifumu wa mbuye wanga mfumu Davide. 38Pamenepo Zadoki wansembe, ndi Natani mneneri, ndi Benaya mwana wa Yehoyada, ndi Akereti, ndi Apeleti aja anatsika, nakweza Solomo pa nyuru ya mfumu Davide, nafika naye ku Gihoni. 39Ndipo Zadoki wansembe anatenga nyanga ya mafuta inali m'Cihema, namdzoza Solomo. Ndipo iwo anaomba lipenga, ndi anthu onse anati, Mfumu Solomo akhale ndi moyo. 40Ndipo anthu onse anakwera namtsata, naliza zitoliro, nakondwera ndi kukondwera kwakukuru, kotero kuti pansi panang'ambikandiphokosolao. 41Ndipo Adoniya ndi oitanidwa onse anali ndi iye analimva atatha kudya. Ndipo Yoabu, pakumva kuomba kwa lipengalo, anati, Phokosolo ndi ciani kuti m'mudzi muli cibumo? 42iye akali cilankhulire, taona, walowa Yonatani mwana wa Abyatara wansembe, ndipo Adoniya anati, Lowa, popeza ndiwe munthu wamphamvu, nubwera nao uthenga wabwino. 43Ndipo Yonatani anayankha, nati kwa Adoniya, Zedi Davide mbuye wathu mfumu walonga Solomo ufumu: 44ndipo mfumu yatumanso Zadoki wansembe, ndi Natani mneneri, ndi Benaya mwana wa Yehoyada, ndi Akereti, ndi Apeleti aja, namkweza iye pa nyuru ya mfumu. 45Ndipo Zadoki wansembe ndi Natani mneneri anamdzoza mfumu ku Gihoni, ndipo acokera kwneneko cikondwerere, ndi m'mudzimo muli phokoso. Ndilo phokoso limene mwamvali. 46Ndiponso Solomo wakhala pa cimpando ca ufumu. 47Ndiponso akapolo a mfumu anadzadalitsa Davide mbuye wathu mfumu, nati, Mulungu wanu aposetse dzina la Solomo lipunde dzina lanu, nakulitse mpando wace wacifumu upose mpando wanu wacifumu; ndipo mfumu anawerama pakamapo. 48Ndiponso watero mfumu, Wolemekezeka Yehova Mulungu wa Israyeli, amene wapereka lero wina wokhala pa mpando wanga wacifumu, maso anga ali cipenyere. 49Pamenepo oitanidwa onse a Adoniya anacita mantha, nanyamuka, napita yense njira yace. 50Ndipo Adoniya anaopa cifukwa ca Solomo, nanyamuka, nakagwira nyanga za guwa la nsembe. 51Ndipo anthu anakauza Solomo, kuti, Taonani, Adoniya aopa mfumu Solomo, popeza taonani, wagwira nyanga za guwa la nsembe, nati, Mfumu Solomo alumbirire ine lero kuti sadzandipha kapolo wace ndi lupanga. 52Ndipo Solomo anati, iye akakhala munthu woyenera silidzagwa pansi tsitsi lace limodzi lonse; koma mukapezeka mwa iye coipa, adzafadi. 53Tsono mfumu Solomo anatuma anthu

nakamtsitsa ku guwa la nsembe. Iye nadza, nagwadira mfumu Solomo; Solomo nati kwa iye, Pita kwanu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Davide atapangira Solomo amwalira

1Pakuyandikira masiku ace a Davide akuti amwalire, analamulira
Solomo mwana wace, nati, 2Ndimuka ine njira ya dziko lonse:
limba mtima tsono, nudzionetse umunthu; 3nusunge cilangizo ca
Yehova Mulungu wako, kuyenda m'njira zace, kusunga malemba
ndi malamulo ndi maweruzo ndi umboni wace, monga
mulembedwa m'cilamulo ca Mose, kuti ukacite mwa nzeru m'zonse
ukacitazo, ndi kumene konse ukatembenukirako; 4kuti Yehova
akakhazikitse mau ace adanenawo za ine, kuti, Ngati ana ako
akasunga bwino njira zao, kuyenda moona pamaso pa Ine ndi
mtima wao wonse ndi moyo wao wonse, nditi sipadzakusowa
mwamuna mmodzi pa mpando wacifumu wa Israyeli. 5Ndiponso
udziwa cimene Yoabu mwana wa Zeruya anandicitira, inde cimene
anawacitira akazembe awiri aja a magulu a nkhondo a Israyeli,
ndiwo Abineri mwana wa Neri, ndi Amasa mwana wa Yeteri, amene
aja anawapha, nakhetsa mwazi ngati wa nkhondo masiku a
mtendere, napaka mwazi wa nkhondo pa lamba lace la m'cuuno
mwace, ndi pa nsapato za pa mapazi ace. 6Cita mwa nzeru yako
tsono, osalola mutu wace waimvi utsikire kumanda ndi
mtendere. 7Koma ucitire zokoma ana amuna aja a Barizilai wa ku
Gileadi, akhale pakati pa akudyera pa gome lako, popeza
momwemo amenewo anandiyandikira muja ndinalikuthawa
Abisalomu mbale wako. 8Ndipo taona uli naye Simeyi mwana wa
Gera wa pfuko la Benjamini wa ku Bahurimu, yemwe uja
adanditemberera ndi temberero lalikuru tsiku lija lakupita ine ku
Mahanaimu; koma anadzakomana ndi ine pa Yordano, ndipo
ndinalumbirira iye pa Yehova, kuti, Sindikupha iwe ndi
lupanga, 9Ndipo tsono, usamuyesera iye wosacimwa, popeza
ndiwe munthu wanzeru, ndipo udziwa umo uyenera kumcitira iye,
nutsitsire mutu wace waimvi ndi mwazi kumanda. 10Ndipo Davide
anagona pamodzi ndi makolo ace, naikidwa m'mudzi wa
Davide. 11Ndipo masiku ace akukhala Davide mfumu ya Israyeli
anali zaka makumi anai; zaka zisanu ndi ziwiri anakhala mfumu ku
Hebroni, ndi zaka makumi atatu mphambu citatu anakhala mfumu
ku Yerusalemu.
12Tsono Solomo anakhala pa mpando wacifumu wa Davide atate
wace, ndipo ufumu wace unakhazikika kwakukuru.

Kulangidwa kwa Adoniya, Abyatara, Yoabu ndi Simeyi

13Pomwepo Adoniya mwana wa Hagati anadza kwa Batiseba amai
wace wa Solomo, ndipo mkaziyo anati, Kodi wadza ndi mtendere?
Nati, Ndi mtendere umene. 14Anatinso, Ndiri nanu mau, Nati iye,
Tanena. 15Nati iye, Mudziwa kuti ufumu unali wanga, ndi kuti
Aisrayeli onse anaika maso ao pa ine, kuti ndikhale mfumu ndine;

koma ufumu watembenuka nukhala wa mbale wanga, popeza iye anaulandira kwa Mulungu. 16Ndipo tsopano, ndikupemphani pempho limodzi, musandikaniza. Ndipo mkaziyo anati kwa iye, Tanena. 17Nati iye, Mundinenere kwa mfumu Solomo, popeza sakukanizani, kuti andipatse Abisagi wa ku Sunamu akhale mkazi wanga. 18Ndipo Batiseba anati, Cabwino, ndidzakunenera kwa mfumu. 19Tsono Batiseba ananka kwa mfumu Solomo kukanenera Adoniya kwa iye. Ndipo mfumu inanyamuka kukomana naye, namuweramira nakhalanso pa mpando wace wacifumu, naikitsa mpando wina wa amace wa mfumu, nakhala iye ku dzanja lace lamanja. 20Pamenepo mkaziyo anati, Ndikupemphani kapempho kamodzi, musandikaniza. Ndipo mfumu inati kwa iye, Tapemphani amai wanga, popeza sindikukanizani. 21Ndipo iye anati, Abisagi wa ku Sunamu apatsidwe kwa Adoniya mbale wanu akhale mkazi wace. 22Ndipo mfumu Solomo anayankha, nati kwa amai wace, Mupempheranji Abisagi wa ku Sunamu akhale wace wa Adoniya? Mumpempherenso ufumu, popeza ndiye mkuru wanga; inde ukhale wace, ndi wa Abyatara wansembeyo, ndi wa Yoabu mwana wa Zeruya. 23Pomwepo mfumu Solomo analumbira pa Yehova, nati, Mulungu andilange naonjezepo, zedi Adoniya wadziphetsa yekha ndi mau awa. 24Ndipo tsono, pali Yehova amene wandikhazikitsa ine, nandikhalitsa pampando wacifumu wa Davide atate wanga, nandimangira nyumba monga analonjeza, zedi Adoniya aphedwa lero lomwe. 25Ndipo mfumu Solomo anatuma dzanja la Benaya mwana wa Yehoyada, ndipo anamgwera, namwalira iye. 26Ndipo mfumu inanena ndi Abyatara wansembeyo, Pita ku Anatoti ku minda yako; pakuti wakutidwa ndi imfa; koma sindikupha iwe lero lino, cifukwa unanyamula likasa la Ambuye Yehova pamaso pa Davide atate wanga, ndi popeza unazunzidwa monse umo atate wanga Davide anazunzidwamo. 27Motero Solomo anacotsa Abyatara asakhalenso wansembe wa Yehova, kuti akakwaniritse mau a Yehova amene aja adalankhula ku Silo za mbumba ya Eli. 28Ndipo mbiriyi inamfika Yoabu, pakuti Yoabu anapambukira kwa Adoniya, angakhale sanapambukira kwa Abisalomu. Ndipo Yoabu anathawira ku cihema ca Yehova, nagwira nyanga za guwa la nsembe. 29Ndipo anamuuza mfumu Solomo, kuti, Yoabu wathawira ku cihema ca Yehova; ndipo taonani, wakhala ku guwa la nsembe. Pomwepo Solomo anatuma Benaya mwana wa Yehoyada, nati, Kamkwereo 30Nafika Benaya ku cihema ca Yehova, nati kwa iye, Mfumu itero, Taturuka. Nati, Iai, koma ndifere pompano. Ndipo Benaya anabweza mau kwa mfumu, nati, Yoabu wanena cakuti, nandiyankha mwakuti mwakuti. 31Ndipo mfumu inati kwa iye, Cita monga umo wanena iye, numkwere, numuike; kuti undicotsere ine ndi nyumba ya atate wanga mwazi uja Yoabu

anaukhetsa wopanda cifukwa. 32Ndipo Yehova adzambwezera mwazi wace pa mutu wace wa iye yekha, popeza iye anawakantha anthu awiri olungama ndi okoma oposa iye mwini, nawapha ndi lupanga, atate wanga Davide osadziwa, ndiwo Abineri mwana wa Neri kazembe wa khamu la nkhondo la Israyeli, ndi Amasa mwana wa Yeteri kazembe wa khamu la nkhondo la Yuda. 33Motero mwazi wao udzabweranso pa mutu wace wa Yoabu, ndi pa mutu wa mbumba yace, ku nthawi yamuyaya; koma Davide, ndi mbumba yace, ndi banja lace, ndi mpando wace wacifumu adzakhala ndi mtendere wa Yehova ku nthawi yamuyaya. 34Pomwepo Benaya mwana wa Yehoyada anakwera namkantha iye, namupha; ndipo anaikidwa m'nyumba yace yace kucipululu. 35Ndipo mfumu inaika Benaya mwana wa Yehoyada m'malo mwace kutsogolera khamu la nkhondo, ndi mfumu inaika Zadoki wansembe m'malo mwa Abyatara. 36Ndipo mfumu inatuma munthu kukaitana Simeyi, nati kwa iye, Udzimangire nyumba m'Yerusalemu, nukhale komweko osaturukako kumka kwina konse. 37Popeza tsiku lomwelo lakuturuka iwe ndi kuoloka mtsinje Kidroni, tadziwa ndithu kuti udzafadi, mwazi wako udzakhala pa mutu wa iwe wekha. 38Ndipo Simeyi ananena ndi mfumu, Mau awa ndi abwino; monga momwe mwanena mbuye wanga mfumu momwemo ndidzacita kapolo wanu. Ndipo Simeyi anakhala m'Yerusalemu masiku ambiri. 39Ndipo kunacitika, zitapita zaka zitatu, kuti akapolo awiri a Simeyi anathawira kwa Akisi mwana wa Maaka mfumu ya Gati. Ndipo anamuuza Simeyi, nati, Taonani, akapolo anu akhala ku Gati. 40Ndipo Simeyi ananyamuka, namangirira mbereko pa buru wace, namka ku Gati kwa Akisi kukafuna aka polo ace; namuka Simeyi, nabwera nao akapolo ace kucokera ku Gati. 41Ndipo anamuuza Solomo, kuti, Simeyi wacoka ku Yerusalemu kumka ku Gati, nabweranso. 42Ndipo mfumu inatuma munthu kukaitana Simeyi, niti kwa iye, Kodi sindinakulumbiritsa pa Yehova ndi kukucenjeza, kuti, Tadziwa ndithu, kuti tsiku lakuturuka iwe ndi kukayenda kwina konse udzafa ndithu? Ndipo iwe unati kwa ine, Mau amene ndawamva ndi abwino. 43Sunasunga cifukwa ninji lumbiro la pa Yehova, ndi lamulo lija ndinakulamulira iwe? 44Tsono mfumu inanenanso ndi Simeyi, Udziwa iwe coipa conse mtima wako umadziwaco, cimene udacitira Davide atate wanga; cifukwa cace Yehova adzakubwezera coipa cako pamutu pako mwini. 45Koma mfumu Solomo adzadalitsika, ndi mpando wacifumu wa Davide udzakhazikika pamaso pa Yehova ku nthawi yamuyaya. 46Pamenepo mfumu inalamulira Benaya mwana wa Yehoyada, ndipo iye anaturuka namkwera, namwalira iye. Ndipo ufumu unakhazikika m'dzanja la Solomo.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Solomo akwatira mwana wa Farao

1Ndipo Solomo anapalana ubwenzi ndi Farao mfumu ya Aigupto,
natenga mwana wamkazi wa Farao, nadza naye ku mudzi wa
Davide, mpaka atamanga nyumba ya iye yekha, ndi nyumba ya
Yehova, ndi linga lozinga Yerusalemu. 2Koma anthu anaphera
nsembe pamisanje, popeza panalibe nyumba yomangira dzina la
Yehova kufikira masiku omwewo. 3Ndipo Solomo anakondana ndi
Yehova, nayenda m'malemba a Davide atate wace; koma anaphera
nsembe nafukiza zonunkhira pamisanje.

Yehova aonekera Solomo m'kulota usiku ku Gibeoni

4Ndipo mfumu inapita ku Gibeoni kukaphera nsembe kumeneko;
popeza msanje waukuru unali kumeneko, Solomo anapereka
nsembe zopsereza cikwi cimodzi pa guwalo la nsembe. 5Ku Gibeoni
Yehova anaonekera Solomo m'kulota usiku, nati Mulungu,
Tapempha cimene ndikupatse. 6Ndipo Solomo anati, Munamcitira
mtumiki wanu Davide atate wanga zokoma zazikulu, monga umo
anayenda pamaso panu ndi coonadi ndi cilungamo ndi mtima
woongoka ndi Inu; ndipo mwamsungira cokoma ici cacikuru kuti
mwampatsa mwana kukhala pa mpando wace wacifumu monga
lero lino. 7Ndipo tsopano, Yehova Inu Mulungu wanga, mwalonga
ine kapolo wanu ufumu m'malo mwa atate wanga Davide, koma
ine ndine kamwana, sindidziwa kuturuka kapena kulowa. 8Ndipo
kapolo wanu ndiri pakati pa anthu anu amene Inu munawasankha,
anthu ambirimbiri osawerengeka, kapena kulembeka m'unyinji
wao. 9Patsani tsono kapolo wanu mtima womvera wakuweruza
anthu anu; kuti ndizindikire pakati pa zabwino ndi zoipa; pakuti
akutha ndani kuweruza anthu anu ambiri amene? 10Ndipo mau
amenewa anakondweretsa Yehova kuti Solomo anapempha
cimeneci. 11Ndipo Mulungu anati kwa iye, Popeza wapempha
cimeneci, osadzipemphera masiku ambiri, osadzipempheranso
cuma, osadzipempheranso moyo wa adani ako, koma
wadzipemphera nzeru zakumvera mirandu; 12taona, ndacita
monga mwa mau ako; taona ndakupatsa mtima wanzeru ndi
wakuzindikira, kotero kuti panalibe wina wolingana ndi iwe kale,
ndipo sadzakhalanso wina wolingana ndi iwe utamuka. 13Ndiponso
zimene sunazipempha adakupatsa, ndipo cuma ndi ulemu, kuti
pakati pa mafumu sipadzakhala yina yolingana ndi iwe masiku ako
onse. 14Ndipo ukadzayenda m'njira zanga kusunga malemba anga
ndi malamulo anga, monga atate wako Davide anayendamo, Ine
ndidzacurukitsa masiku ako. 15Ndipo Solomo anauka, ndipo taona,
ndilo loto; nabwera ku Yerusalemu, naima ku likasa la cipangano ca
Yehova, napereka nsembe zopsereza ndi nsembe zamtendere,
nakonzera anyamata ace onse madyerero.

Solomo aweruza mlandu wa akazi awiri aja

16Pamenepo analowa kwa mfumu akazi awiri, ndiwo adama, naima
pamaso pace. 17Ndipo mkazi mmodzi anati, Mbuye wanga, ine ndi
mkazi uyu tikhala awiri m'nyumba imodzi; ndipo ine ndinaona
mwana, iye ali m'nyumbamo. 18Ndipo kunacitika kuti tsiku lacitatu
nditaona ine mwana, mnzangayu anaonanso mwana; ndipo ife
tinali pamodzi, munalibe mlendo ndi ife m'nyumbamo, koma ife
awiri m'nyumbamo. 19Ndipo mwana wa mnzangayu anamwalira
usiku, pokhala iyeyu anamgonera. 20Ndipo iye anauka pakati pa
usiku, natenga mwana wanga kumimba kwanga, mdzakazi wanu
ndiri m'tulo, namuika m'mfukato mwace, naika mwana wace
wakufa m'mfukato mwanga. 21Ndipo pouka ine m'mawa
kuyamwitsa mwana wanga ndaona ngwakufa, koma
nditamzindikira m'mawa ndaona si mwana wanga wobala ine
ai. 22Ndipo mkazi winayo anati, lai, koma wamoyoyu ndi mwana
wanga, ndi wakufayu ndi mwana wako. Ndipo uja anati, lai, koma
wakufayu ndi mwana wako, ndi wamoyoyu ndi mwana wanga.
Motero iwo analankhula pamaso pa mfumu. 23Tsono mfumu inati,
Uyu akuti, Wamoyoyu ndiye mwana wanga ndi wakufayu ndiye
mwana wako; ndipo winayo akuti, lai, koma mwana wako ndiye
wakufayu, ndi mwana wanga ndiye wamoyoyu. 24Niti mfumu,
Kanaitengereni cimpeni. Ndipo iwo anabwera ndi cimpeni kwa
mfumu. 25Mfumu niti, Dula pakati mwana wamoyoyu, nupatse
mmodzi cipinjiri, ndi wina cipinjiri cace. 26Koma mkazi amene
mwana wamoyo anali wace analankhula ndi mfumu, popeza mtima
wace unalira mwana wace, nati, Ha! mbuye wanga, mumpatse uyo
mwana wamoyo osamupha konse. Koma winayo anati, Asakhale
wanga kapena wako, dulani. 27Pamenepo mfumu inayankha, niti,
Mumpatse wacifundoyo mwana wamoyo, osamupha konse, uyo
ndiye amace. 28Ndipo Aisrayeli onse anamva maweruzidwe ace
idaweruza mfumu, naopa mfumu; pokhala anaona kuti nzeru ya
Mulungu inali mwa iye yakuweruza.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Nduna za Solomo, ukuru wa ufumu wace

1Ndipo mfumu Solomo anali mfumu ya Israyeli yense. 2Ndipo akuru a mfumu
ndi awa: Azariya mwana wa Zadoki anali nduna, 3Elihorepa ndi Ahiya ana a
Sisa alembi, Yehosafati mwana wa Ahiludi wolembera mbiri, 4ndi Benaya
mwana wa Yehoyada anali kazembe wa nkhondo, ndi Zadoki ndi Abyatara
anali ansembe, 5ndi Azariya mwana wa Natani anayang'anira akapitao, ndi
Zabudi mwana wa Natani anali nduna yopangira mfumu, 6ndi Ahisara
anayang'anira banja la mfumu, ndi Adoniramu mwana wa Abida anali
wamsonkho. 7Ndipo Solomo anali nao akapitao khumi ndi awiri akuyang'anira
Aisrayeli onse, akufikitsira mfumu ndi banja lace zakudya; ali yense anafikitsa
zakudya zofikira mwezi umodzi wa caka. 8Ndipo maina ao ndiwo: Benhuri
anatengetsa ku mapiri a Efraimu; 9Bendekeri ku Makazi ndi Saalibimu ndi
Betsemesi ndi Elonibetanani; 10Benhesedi ku Aruboti ndi Soko ndi dziko lonse
la Heferi; 11Benabinadabu ku mtunda wa Dori, mkazi wace ndiye Tafati
mwana wa Solomo; 12Baana mwana wa Ahiludi ku Tanaki ndi Megido ndi
Betseani konse, ali pafupi ndi Zaratana kunsi kwa Yezreeli, kuyambira ku
Betseani kufikira ku Abelimehola, kufikiranso kundunji ku
Yokineamu; 13Benigeheri ku Ramoti Gileadi, iyeyo anali nayo midzi ya Yairo
mwana wa Manase iri m'Gileadiyo, iye anali nalo dziko la Arigobi liri m'Basani,
midzi yaikuru makumi asanu ndi limodzi yamalinga ndi zitseko
zamkuwa; 14Abinadabu mwana wa Ido ku Nahanaimu; 15Ahimazi ku Nafitali,
iyeyu adakwatira Basemati mwana wa Solomo; 16Baana mwana wa Husayi ku
Aseri ndi ku Aloti; 17Yehosafati mwana wa Paruwa ku Isakara; 18Simeyi
mwana wa Ela ku Benjamini; 19Geberi mwana wa Uri ku dziko la Gileadi, dziko
la Sihoni mfumu ya Aamori, ndi la Ogi mfumu ya Basani; munalibe kapitao
wina m'deramo. 20Ayuda ndi Aisrayeli anacuruka ngati mcenga wa kunyanja,
namadya namamwa namakondwera.
21Ndipo Solomo analamulira maiko onse, kuyambira ku Firate kufikira ku dziko
la Afilisti ndi ku malire a Aigupto; anthu anabwera nayo mitulo namtumikira
Solomo masiku onse a moyo wace. 22Ndipo zakudya za Solomo zofikira tsiku
limodzi zinalr miyeso makumi atatu ya ufa wosalala, ndi miyeso makumi
asanu ndi limodzi ya ufa wamankhupete, 23ng'ombe zonenepa khumi, ndi
ng'ombe za kubusa makumi awiri, ndi nkhosa zana limodzi, osawerenganso
ngondo ndi nswala ndi mphoyo ndi mbalame zoweta. 24Pakuti analamulira
dziko lonse liri tsidya lino la Firate, kuyambira ku Tipsa kufikira ku Gaza, inde
mafumu onse a ku tsidya tino la Firate; nakhala ndi mtendere kozungulira
konseko, 25Ndipo Ayuda ndi Aisrayeli anakhala mosatekeseka, munthu yense
patsinde pa mpesa wace ndi mkuyu wace, kuyambira ku Dani mpaka ku
Beeriseba, masiku onse a Solomo. 26Ndipo Solomo anali nazo zipinda za
akavalo a magareta ace zikwi makumi anai, ndi apakavalo zikwi khumi
mphambu ziwiri. 27Ndipo akapitao aja anatengetsera cakudya Solomo ndi
anthu onse akudya ku gome la mfumu Solomo, munthu yense m'mwezi
mwace, sanalola kanthu kasoweke. 28Barelenso ndi udzu wa akavalo ndi
ngamila anabwera nazo kumalo kwao, munthu yense monga momwe
anamuuzira.

Nzeru ya Solomo

29Ndipo Mulungu anampatsa Solomo nzeru ndi luntha lambiri, ndi mtima
wodziwa za mitundu mitundu, zonga mcenga uli m'mbali mwa
nyanja. 30Ndipo nzeru ya Solomo inaposa nzeru za anthu onse a kum'mawa,
ndi nzeru zonse za ku Aigupto. 31Pakuti anali wanzeru woposa anthu onse,
woposa Etani wa ku Ezra, ndi Hemani, ndi Kalikoli, ndi Darida ana a Maholi;

ndipo mbiri yace inafikira amitundu onse ozungulira. 32Ndipo ananena miyambo zikwi zitatu, ndipo nyimbo zace zinali cikwi cimodzi mphambu zisanu. 33Nakamba za mitengo, kuyambira mkungudza uli ku Lebano kufikira hisopi wophuka pakhoma; anakambanso za nyama ndi mbalame ndi zinthu zokwawa pansi ndi za nsomba. 34Ndipo anafikako anthu a mitundu yonse kudzamva nzeru ya Solomo, ocokera kwa mafumu onse a dziko lonse lapansi, amene adamva mbiri ya nzeru yace.

Solomo apangana ndi Hiramu za mirimo vomansa nayo Kacisi

1Ndipo Hiramu mfumu ya ku Turo anatuma anyamata ace kwa
Solomo, popeza anamva kuti adamdzoza mfumu m'malo mwa
atate wace; pakuti Hiramu adakondana ndi Davide masiku
onse. 2Ndipo Solomo anatumiza mau kwa Hiramu, nati, 3Mudziwa
inu kuti atate wanga Davide sanathe kumangira dzina la Yehova
Mulungu wace nyumba, cifukwa ca nkhondo zakumzinga konseko,
mpaka atawaika Yehova pansi pa mapazi ace. 4Koma tsopano
Yehova Mulungu wanga wandipumulitsa ku mbali zonse; palibe
wotsutsana nane, kapena coipa condigwera. 5Ndipo taonani,
ndikuti ndimangire dzina la Yehova Mulungu wanga nyumba,
monga Yehova anauza atate wanga Davide, ndi kuti, Mwana wako
ndidzamuika pa mpando wako wacifumu m'malo mwako, iyeyo
adzamangira dzina langa nyumbayo. 6Ndipo tsono, lamulirani kuti
anditemere mitengo yamkungudza ku Lebano, ndipo akapolo anga
adzakhala ndi akapolo anu, ndipo ndidzakupatsani mphotho ya
akapolo anu monga mudzanena; popeza mudziwa kuti pakati pa
ife palibe mmisiri wakudziwa kutema mitengo ngati anthu a ku
Sidoni. 7Ndipo kunacitika, pamene Hiramu anamva mau ace a
Solomo, anakondwera kwakukuru, nati, Alemekezeke Yehova lero
amene wampatsa Davide mwana wanzeru akhale mfumu ya anthu
aunyinji amenewa. 8Ndipo Hiramu anatumiza kwa Solomo, nati,
Ndazimva zija munatumiza kwa inezo, ndidzacita cifuniro canu
conse, kunena za mitengo yamkungudza ndi mitengo
yamlombwa. 9Akapolo anga adzatsika nayo ku Lebano kufika nayo
ku nyanja yamcere, ndipo ine ndidzaiyandamitsa paphaka kufikira
komwe mudzandiuzako, ndi kumeneko ndidzaimasula, ndipo
mudzaitenga; nimudzacita cifuniro canga, kumapatsa banja langa
zakudya. 10Tsono Hiramu anapatsa Solomo mitengo yamkungudza
ndi mitengo yamlombwa monga momwe anafuniramo. 11Ndipo
Solomo anapatsa Hiramu miyeso ya tirigu zikwi makumi awiri
ndiyo zakudya za banja lace, ndi miyeso makumi awiri ya mafuta
oyera; motero Solomo anapatsa Hiramu caka ndi caka. 12Ndipo
Yehova anapatsa Solomo nzeru monga momwe adamlonjezera;
ndipo panali mtendere pakati pa Hiramu ndi Solomo, iwo awiri
napangana pamodzi.
13Ndipo mfumu Solomo anasonkhetsa athangata mwa Aisrayeli
onse, ndi athangatawo ndiwo anthu zikwi makumi atatu. 14Ndipo
anawatuma ku Lebano mwezi umodzi zikwi khumi kuwasintha,
mwezi umodzi iwo anali ku Lebano, miyezi iwiri anali kwao; ndipo
Adoniramu anali kapitao wa athangata. 15Ndipo Solomo
anawasenzetsa akatundu anthu zikwi makumi asanu ndi awiri, ndi

anthu zikwi makumi asanu ndi atatu anatema
m'mapiri; 16osawerenga akapitao a Solomo akuyang'anira nchito,
ndiwo zikwi zitatu mphambu mazana atatu, amenewo analamulira
anthu aja akugwira nchito. 17Ndipo mfumu inalamula iwo, natuta
miyala yaikuru-ikuru ya mtengo wapatali, kuika maziko ace a
nyumbayo ndi miyala yosemasema. 18Ndipo omanga nyumba a
Solomo ndi omanga nyumba a Hiramu ndi anthu a ku Gebala
anaisema, naikonza mitengo ndi miyala yakumangira nyumbayo.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Za mamangidwe a Kacisi

1Ndipo kunacitika zitapita zaka mazana anai mphambu makumi
asanu ndi atatu ataturuka ana a Israyeli m'dziko la Aigupto, caka
cacinai cakukhala Solomo mfumu ya Israyeli, m'mwezi wa Zivi,
ndiwo mwezi waciwiri, iye anayamba kumanga nyumba ya
Yehova. 2Ndipo nyumbayo mfumu Solomo anaimangira Yehova,
m'litali mwace munali mikono makumi asanu ndi limodzi, ndi
m'mimba mwace mikono makumi awiri, ndi msinkhu wace mikono
makumi atatu. 3Ndipo anamanga likole pakhomo pa nyumba ya
kacisiyo, m'litali mwace munali mikono makumi awiri monga
m'mimba mwace mwa nyumbayo, kupingasa kwace kunali mikono
khumi ku khomo la nyumba. 4Ndipo m'nvumbamo anamanga
mazenera a made okhazikika. 5Ndipo anamanga zipinda
zosanjikizana zogundana ndi khoma, kuzungulira makoma a
nyumba ya Kacisi, ndi monenera momwemo; namanga zipinda
zozinga, 6Cipinda capansico kupingasa kwace kunali mikono isanu,
capakatico kupingasa kwace mikono isanu ndi umodzi, cacitatuco
kupingasa kwace mikono isanu ndi iwiri; pakuti kubwalo anacepsa
khoma pozungulirapo, mitanda isalongedwe m'makoma a
nyumba. 7Ndipo nyumbayo pomangidwa inamangidwa ndi miyala
yokonzeratu asanaitute; ndipo m'nyumbamo simunamveka: kulira
nyundo, kapena nkhwangwa, kapena cipangizo cacitsulo,
pomangidwa iyo. 8Khomo lolowera m'zipinda za pakati linali ku
mbali ya ku dzanja lamanja ya nyumba; ndipo anthu amakwerera
pa makwerero ozunguniza, kutikira ku zipinda za pakati, ndi
kuturuka m'zapakatizo kulowa m'zacitatuzo, 9Momwemo
anamanga nyumbayo naitsiriza, naika mitanda, naifolera ndi
matabwa amikungudza. 10Ndipo anamanga zipindazo zogundana
ndi nyumba yonseyo, cipinda ciri conse msinkhu wace mikono
isanu; ndipo anazilumikizitsa kunyumba ndi mitengo
yamkungudza.
11Ndipo mau a Yehova anafika kwa Solomo, nati, 12Kunena za
nyumba yino ulikuimanga, ukamayenda iwe m'malemba anga, ndi
kumacita maweruzo anga, ndi kumasunga malamulo anga onse
kuyendamo, pamenepo Ine ndidzakhazikitsira iwe mau anga
amene ndinauza Davide atate wako. 13Ndipo ndidzakhala pakati pa
ana a Israyeli osawasiya anthu anga a Israyeli.
14Tsono Solomo anamanga nyumbayo naitsiriza. 15Ndipo anacinga
makoma a nyumba m'katimo ndi matabwa amkungudza,
kuyambira pansi kufikira posanja, nacinga m'katimo ndi matabwa,
nayala pansi m'nyumbamo matabwa amlombwa. 16Ndipo
anadulitsa ndi matabwa amkungudza mikono makumi awiri m'kati
mwa nyumba m'tsogolo mwace, kuyambira pansi kulekeza

kumitanda; ici anamanga m'katimo cikhale monenera, malo opatulikitsa. 17Ndipo nyumbayo, ndiyo Kacisi wa cakuno ca monenera, inali ya mikono makumi anai. 18Ndipo m'kati mwa nyumba munali mikungudza yosemasema, ngati zikho ndi maluwa oti gada; munali mikungudza yokha yokha simunaoneka mwala ai, 19Ndipo anakonza monenera m'kati mwa nyumba m'tsogolo mwace, kuikamo likasa la cipangano la Yehova. 20Ndipo m'kati mwa monenera m'menemo, m'litali mwace munali mikono makumi awiri, kupingasa kwace mikono makumi awiri, ndi msinkhu wace mikono makumi awiri; ndipo anamukuta ndi golidi woyengetsa, nakutanso guwa la nsembe ndi matabwa amkungudza, 21Momwemo Solomo anakuta m'kati mwa nyumba ndi golidi woyengetsa, natambalika maunyolo agolidi cakuno ca monenera, namukuta ndi golidi. 22Ndipo nyumba yonse anaikuta ndi golidi mpaka adatha nyumba yonse, ndi guwa lonse la nsembe linali cakuno ca monenera analikuta ndi golidi. 23Ndipo m'moneneramo anasema mitengo yaazitona akerubi awiri, yense wa msinkhu wace mikono khumi. 24Ndipo phiko limodzi la kerubi linali la mikono isanu, ndi phiko lina la kerubi linalinso la mikono isanu; kuyambira ku nsonga ya phiko limodzi kufikira ku nsonga ya phiko lina inali mikono khumi. 25Ndi kerubi winayo msinkhu wace unali mikono khumi; akerubi onse awiri anafanana muyeso wao ndi msinkhu wao. 26Msinkhu wa kerubi mmodzi unali mikono khumi, ndi wa kerubi wina momwemo. 27Ndipo anaika akerubiwo m'cipinda ca m'katimo, ndi mapiko a akerubiwo anatambasuka kotero kuti phiko lace la kerubi mmodzi linajima ku khoma limodzi, ndipo phiko la kerubi wina linajima khoma lina, ndi mapiko ao anagundana pakati pa nyumba. 28Ndipo anawakuta akerubi ndi golidi. 29Nalemba m'makoma onse akuzinga cipinda mafano olemba ngati akerubi ndi migwalangwa ndi maluwa oti gada, m'katimo ndi kumbuyo kwace. 30Ndipo anakuta ndi golidi pansi pace pa nyumba m'katimo ndi kunja. 31Ndipo pa khomo la monenera anapanga zitseko za mtengo waazitona, citando ca khomolo cinali limodzi la magawo asanu a khoma lace. 32Zitseko ziwiri zomwe zinali za mtengo waazitona, anasemapo ngati akerubi ndi migwalangwa ndi maluwa oti gada, nawakuta ndi golidi; inde anakutanso ndi golidi akerubi ndi migwalangwayo. 33Momwemo anapanganso mphuthu zaazitona za pa khomo la Kacisi, citando cace cinali limodzi la magawo anai a khoma; 34ndi zitseko ziwiri za mitengo yamlombwa pa khomo lina; panali citseko copatukana, ndi pa linzace panali citseko copatukana, 35Ndipo analembapo ngati akerubi ndi migwalangwa ndi maluwa oti gada, nakuta zolembazo ndi golidi wopsyapsyala, 36Ndipo bwalo la m'kati analimanga mizere itatu ya miyala yosemasema, ndi mzere umodzi wa

mitanda yamkungudza. 37Maziko ace a nyumba ya Mulungu
anaikidwa m'caka cacinai m'mwezi wa Zivi. 38Ndipo m'caka
cakhumi ndi cimodzi m'mwezi wa Buli ndiwo mwezi wacisanu ndi
citatu anatsiriza nyumba konse konse monga mwa mamangidwe
ace onse. Momwemo anaimanga zaka zisanu ndi ziwiri.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Mamangidwe a nyumba Yd Solomo

1Koma nyumba ya iye yekha Solomo anaimanga zaka khumi
mphambu zitatu, natsiriza nyumba yace yonse. 2Anamanganso
nyumba yochedwa Nkhalango ya Lebano, m'litali mwace munali
mikono zana limodzi, kupingasa kwace mikono makumi asanu, ndi
msinkhu wace mikono makumi atatu; naisanja pa mizere inai ya
mapanda amkungudza, ndi mitanda yamkungudza yotanthalika
mapandawo. 3Ndipo inayalidwa ndi mkungudza pamwamba pa
zipinda makumi anai mphambu zisanu zolongosoledwa pa
mapanda, mzere umodzi zipinda khumi mphambu asanu. 4Ndipo
panali mazenera m'mizere itatuyo, zenera limodzi lopenyana ndi
linzace mizere itatu. 5Ndipo makomo onse ndi mphuthu zonse
zinali zamphwamphwa maonekedwe ace, ndipo zenera limodzi
linapenyana ndi linzace mizere Itatu. 6Ndipo anamanga khumbi la
nsanamira, m'litali mwace munali mikono makumi asanu,
kupingasa kwace mikono makumi atatu; ndipo panali khumbi lina
patsogolo pace, ndi nsanamira ndi mitanda patsogolo
pacepo. 7Ndipo anamanga khumbi la mpando wacifumu
loweruziramo iye, ndilo khumbi la mirandu, ndipo linayalidwa ndi
mkungudza pansi ndi posanja. 8Ndipo nyumba yace yakukhalamo
iye, m'bwalo lina la m'tsogolo mwa khumbilo, linamangidwa
cimodzimodzi. Anammangiranso nyumba mwana wamkazi wa
Farao, amene adamkwatira Solomo, yofanafana ndi khumbi
limeneli. 9Izi zonse zinali za miyala ya mtengo wapatali
yosemasema, ya muyeso muyeso, yoceka ndi mipeni ya mano
mana m'katimo ndi kunjako, kuyambira kumazikokufikira kumutu,
momwemonso kunjako ku bwalo lalikuru, 10Ndipo maziko ace anali
a miyala ya mtengo wapatali, ndiyo miyala yaikulu, miyala ya
mikono khumi, ndi miyala ya mikono isanu ndi itatu. 11Ndi
pamwamba pace panali miyala ya mtengo wapatali, ndiyo miyala
yosemasema monga muyeso wace, ndi mitengo
yamkungudza. 12Ndipo bwalo lalikuru lozingapo linali ndi mizere
itatu ya miyala yosemasema, ndi mzere umodzi wa mitanda
yamkungundza, monga bwalo la pakati pa nyumba ya Yehova, ndi
likole la nyumbayo.

Zokometsera ndi zipangizo za Kacisi

13Ndipo mfumu Solomo anatuma anthu kukatenga Hiramu ku
Turo. 14Iyeyo anali mwana wace wa mkazi wamasiye wa pfuko la
Nafitali, atate wace anali munthu wa ku Turo, mfundi wa mkuwa;
ndipo iye anadzala ndi nzeru ndi luntha ndi luso kugwira nchito
zonse za mkuwa. Ndipo anadza kwa mfumu Solomo namgwirira
nchito zace zonse. 15Popeza iyeyu anaunda nsanamira ziwiri
zamkuwa, msinkhu wace wa imodzi unali mikono khumi mphambu

isanu ndi itatu; ndipo cingwe ca mikono khumi mphambu iwiri cinayesa thupi la nsanamira imodzi. 16Ndipo anapanga mitu iwiri ya mkuwa wosungunula, kulika pamwamba pa nsanamirazo, msinkhu wace wa mutu wina unali mikono isanu, ndi msinkhu wa mutu unzace mikono isanu. 17Ndipo panali maukonde olukaluka ndi zoyangayanga, zokolana za pa mitu imene inali pamwamba pa nsanamira; zisanu ndi ziwiri za pa mutu wina, ndi zisanu ndi ziwiri za pa mutu unzace. 18M'mwemo anapanga nsanamira, ndipo panali mizere iwiri yozungulira ukonde umodzi, kukuta ndi makangaza mituyi inali pamwambapo, nacita momwemo ndi mutu winawo. 19Ndipo mituyi inali pamwamba pa nsanamira za pa likole inali ngati akakombo malembedwe ace, a mikono inai. 20Ndipo panalinso mitu pamwamba pa nsanamira ziwirizo, pafupi pa mimbayo, inali m'mbali mwace mwa ukondewo; ndipo makangazawo anali mazana awiri, akukhala mizere yozinga nda nda mutu winawo. 21Ndipo anaimiritsa nsanamirazi pa likole la Kacisi; naimiritsa nsanamira ya ku dzanja lamanja, nacha dzina lace Yakini; naimiritsa nsanamira yakumanzere, nacha dzina lace Boazi. 22Ndipo pamwamba pa nsanamirazo panali ngati akakombo malembedwe ace; motero anaitsiriza nchito ya nsanamirazo. 23Ndipo anayenganso thawale lamkuwa, kukamwa kwace kunali kwa mikono khumi, linali lozunguniza, ndi msinkhu wace unali mikono isanu; ndi cingwe ca mikono makumi atatu cinalizungulira. 24Ndipo m'khosi mwace munali ngati zikho zozinganiza m'mkono umodzi zikho khumi zakuzinganiza thawalelo; zikhozo zinayengedwa m'mizere iwiri poyengedwa thawalelo. 25Linasanjikika pa ng'ombe khumi mphambu ziwiri, zitatu zinapenya kumpoto, zitatu kumadzulo, zitatu kumwera, zitatu kum'mawa; ndipo thawalelo linakhazikika pamwamba pa izo; ndipo nkholo zao zinayang'anana. 26Ndipo kucindikira kwace kunali ngati m'manja mwa munthu, ndipo mlomo wace unasadamuka ngati mlomo wa comwera, ngati maluwa akakombo, analowamo madzi a mitsuko yaikuru zikwi ziwiri. 27Ndipo anapanga maphaka khumi amkuwa, m'litali mwace mwa phaka limodzi mikono inai, ndi kupingasa kwace mikono inai, ndi msinkhu wace mikono itatu. 28Ndipo mapangidwe a maphakawo anali otere: anali nao matsekerezo ao, ndipo matsekerezo anali pakati pa mbano. 29Ndipo pa matsekerezo a pakati pa mbano panali ngati mikango ndi ng'ombe ndi akerubi, ndi pamwamba pa mbano panali cosanjikirapo; ndipo pansi pa mikango ndi ng'ombe panaphatikizika zotsetseremba zoyangayanga zokoloweka. 30Ndipo phaka lid lonse linali ndi njinga zamkuwa zinai ndi mitanda yamkuwa, ndipo ngondya zace zinai zinali ndi mapewa; pansi pa thawale panali mapewa oyengeka pa mbali pa zophatikizika

zonse. 31Ndipo pakamwa pace m'katimo pamwamba pa
cosanjikira, panayesa mkono umodzi; koma pakamwa pace panali
posadamuka, monga mapangidwe ace a cosanjikira, mkono
umodzi ndi nusu; ndiponso pakamwa pace panali zolemba ndi
matsekerezo ace anali amphwamphwa, si ozunguniza. 32Ndipo
njinga zinai zinali pansi pa matsekerezo, ndi mitanda ya njinga
inali m'mphakamo, ndi msinkhu wa njinga imodzi unali mkono
umodzi ndi nusu. 33Ndipo mapangidwe a njinga analingana ndi
mapangidwe a njinga za gareta, mitanda yace ndi mkombero wace
ndi nthiti zace ndi mtima wace zonsezo zinayengedwa. 34Ndipo
panali ngati mapewa anai pansi pa ngondya zinai za phaka
limodzi, mapewawo anali a phaka lomwelo. 35Ndipo pamwamba pa
phaka panali khoma lozunguniza, msinkhu wace nusu ya mkono;
ndi pamwamba pa phaka panali mbano zace ndi matsekerezo a
phaka lomwelo. 36Ndipo m'mapanthi mwa mbano zace ndi pa
matsekerezo ace analemba ngati akerubi ndi mikango ndi
migwalangwa, monga mwa malo ace a zonsezo, ndi zoyangayanga
zozungulira. 37Motero anapanga maphaka khumiwo, anafanana
mayengedwe ao muyeso wao ndi maonekedwe ao. 38Ndipo
anapanga mbiya zamphwamphwa khumi zamkuwa; m'mbiya
imodziyo munalowamo madzi a mitsuko yaikuru makumi anai,
ndipo mbiya iri yonse inali ya mikono inai: pa phaka liri lonse la
maphaka aja khumi panakhala mbiya imodzi. 39Ndipo anaika
maphaka asanu ku dzanja lamanja la nyumba, ndi maphaka asanu
ku dzanja lamanzere la nyumba; naika thawalelo ku dzanja
lamanja la nyumba kum'mawa kupenya kumwera. 40Ndipo Hiramu
anayenga mbiyazo ndi zoolera ndi mbale zowazira. Motero Hiramu
anatsiriza kupanga nchito yonse anaicitira mfumu Solomo ya
m'nyumba ya Yehova. 41Nsanamira ziwirizo, ndi mbale za mitu inali
pamwamba pa nsanamira ziwirizo, ndi maukonde awiri ophimbira
mbale ziwiri za mitu inali pamwamba pa nsanamirazo, 42ndi
makangaza mazana anai a maukonde awiriwo, mizere iwiri ya
makangaza a ukonde umodzi kuphimbira mbale ziwiri za mitu inali
pa nsanamirazo, 43ndi maphaka khumiwo ndi mbiya khumi ziri pa
maphakawo, 44ndi thawale limodzilo, ndi ng'ombe khumi
mphambu ziwirizo pansi pa thawale; 45ndi miphikayo, ndi
zoolerazo, ndi mbalezo; inde zotengera zonse zimene Hiramu
anampangira mfumu Solomo za m'nyumba ya Yehova, zinali za
mkuwa wonyezimira. 46Mfumu inaziyenga pa cidikha ca ku
Yordano, m'dothe ladongo, pauti pa Sukoti ndi Zaritani. 47Ndipo
Solomo anazileka zipangizo zonse osaziyesa, popeza zinacuruka
ndithu; kulemera kwace kwa mkuwa wonsewo
sikunayeseka. 48Ndipo Solomo anapanga zipangizo zonse za
m'nyumba ya Mulungu: guwa la nsembe lagolidi, ndi gome lagolidi

loikapo mikate yoonekera; 49ndi zoikapo nyali za golidi
woyengetsa, zisanu ku dzanja lamanja, zisanu kulamanzere,
cakuno ca monenera, ndi maluwa ndi nyali ndi mbano
zagolidi; 50ndi zikho, ndi zozimira nyali, ndi mbale, ndi zipande, ndi
zopalira mota za golidi woyengetsa, ndi zomangira zitseko zagolidi,
za zitseko za cipinda ca m'katimo, malo opatulikitsa, ndiponso za
zitseko za nyumba ya Kacisi. 51Motero nchito zonse zinatsirizika,
zimene mfumu Solomo anacitira nyumba ya Yehova. Ndipo Solomo
analonga zinthu adazipatula Davide atate wace, ndizo siliva ndi
golidi ndi zipangizo zomwe naziika mosungira cuma ca nyumba ya
Yehova.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Aika likasa m'Kacisi

1Pamenepo Solomo anasonkhanitsa akulu a Israyeli, ndi akulu onse
a mafuko, akalonga a nyumba za atate a ana a Israyeli, kwa
mfumu Solomo m'Yerusalemu, kukatenga likasa la cipangano ca
Yehova m'mudzi wa Davide, ndiwo Ziyoni. 2Ndipo anthu onse a
Israyeli anasonkhana kwa mfumu Solomo kukadyereram'mwezi wa
Etanimu, ndiwo mwezi wacisanu ndi ciwiri. 3Ndipo akulu onse a
Israyeli anadza, ansembe nanyamula likasa. 4Ndipo anatenga
likasa la Yehova, ndi cihema cokomanako, ndi zipangizo zonse
zopatulika, zinali m'cihemamo, inde zimenezi anazitenga ansembe
ndi Alevi. 5Ndipo mfumu Solomo ndi msonkhano wonse wa Israyeli
wosonkhana kwa iye anali naye kulikasa, naphera nkhosa ndi
ng'ombe za nsembe zosawerengeka ndi zosadziwika, cifukwa ca
unyinji wao. 6Ndipo ansembe analonga likasa la cipangano ca
Yehova kumalo kwace, ku monenera mwa nyumba, ku malo
opatulikitsa, munsi mwa mapiko a akerubi, 7Popeza akerubiwo
anatambasula mapiko ao awiri pamwamba pa likasa, ndipo
akerubiwo anaphimba pamwamba pa likasa ndi mphiko
zace. 8Ndipo mphikozo zinatalika kuti nsonga za mphiko zidaoneka
ku malo opatulika cakuno ca monenera; koma sizinaoneka
kubwalo; ndipo zikhala pomwepo mpaka lero lino. 9Munalibe
kanthu m'likasamo koma magome awiri aja amwala Mose
anawalongamo pa Horebu, pamene Yehova anapangana ndi ana a
Israyeli, poturuka iwo m'dziko la Aigupto. 10Ndipo kunacitika
atāturuka ansembe m'malo opatulika, mtambo unadzaza nyumba
ya Yehova, 11ndipo ansembe sanakhoza kuimirira kurumikira
cifukwa ca mtambowo, popeza ulemerero wa Yehova
unadzazanyumba ya Yehova.

Mau a Saloma popereka Kacisi kwa Mulungu

12Pamenepo Solomo anati, Yehova ananena kuti adzakhala
m'mdima waukuru. 13Ine ndakumangirani ndithu nyumba
yokhalamo Inu, ndiyo malo okhalamo inu nthawi zosatha. 14Ndipo
mfumu inapotoloka nkhope yace, nidalitsa msonkhano wonse wa
Israyeli, Ndi msonkhano wonse wa Israyeli unaimirira. 15Nati iye,
Wolemekezeka ndi Yehova Mulungu wa Israyeli amene analankhula
m'kamwa mwace ndi Davide atate wanga, nakwaniritsa ndi dzanja
lace, nati, 16Kuyambira tsiku lakuturutsa Ine anthu anga Aisrayeli
m'dziko la Aigupto, sindinasankha mudzi uli wonse mwa mafuko
onse a Israyeli kumangamo nyumba yokhalamo dzina langa, koma
ndinasankha Davide kukhala mfumu ya anthu anga
Aisrayeli. 17Ndipo Davide atate wanga anafuna m'mtima mwace
kumangira dzina la Yehova Mulungu wa Israyeli nyumba. 18Koma
Yehova ananena ndi Davide atate wanga, Popeza unafuna

m'mtima mwako kumangira dzina langa nyumba, unacita bwino kuti m'mtima mwako unatero. 19Koma usamange ndiwe nyumbayo, koma mwana wako adzaturuka m'cuuno mwako, iyeyo adzamangira dzina langa nyumba. 20Ndipo Yehova wakhazikitsa mau ace analankhulawo, ndipo ndauka ndine m'malo mwa Davide atate wanga, ndipo ndikhala pa mpando wacifumu wa Israyeli monga adalonjeza Yehova, ndipo ndamangira dzina la Yehova Mulungu wa Israyeli nyumba. 21Ndipo ndakonzera malo likasalo, m'mene muli cipangano ca Yehova, cimene anapangana ndi makolo athu pamene anawaturutsa m'dziko la Aigupto.
22Ndipo Solomo anaimirira ku guwa la nsembe la Yehova pamaso pa msonkhano wonse wa Israyeli, natambasulira manja ace kumwamba, nati, 23Yehova Mulungu wa Israyeli, palibe Mulungu wolingana ndi inu m'thambo la kumwamba, kapena pa dziko lapansi, wakusungira cipangano ndi cifundo akapolo anu akuyenda ndi mtima wonse pamaso panu, 24wakusungira mtumild wanu Davide atate wanga cimene mudamlonjezaco; munalankhulanso m'kamwa mwanu ndi kukwaniritsa ndi dzanja lanu monga lero lino. 25Ndipo tsopano, Yehova Mulungu wa Israyeli, msungireni mtumiki wanu Davide atate wanga cimene cija mudamlonjezaco, ndi kuti, Sadzakusowa munthu pamaso panga wokhala pa mpando wacifumu wa Israyeli; komatu ana ako acenjere njira yao, kuti akayende pamaso panga monga umo unayendera iwe pamaso panga. 26Ndipo tsopano, Mulungu wa Israyeli, atsimikizike mau anu amene munalankhula ndi mtumiki wanu Davide atate wanga.
27Kodi Mulungu adzakhala ndithu pa dziko lapansi? Taonani, thambo ndi m'Mwambamwamba zicepa kukulandirani, koposa kotani nanga nyumba iyi ndaimangayi. 28Koma muceukire pemphero la kapolo wanu, ndi pembedzero lace, Yehova Mulungu wanga, kumvera kulira ndi kupempha kwace kumene kapolo wanu apempha pamaso panu lero; 29kuti maso anu atsegukire nyumba yino usiku ndi usana, kumalo kumene munanenako, Dzina langa lidzakhala komweko; kuti mumvere pemphero limene adzapemphera kapolo wanu lolunjika kumalo kuno. 30Ndipo mverani pembedzero la kapolo wanu ndi la anthu anu Aisrayeli, pamene adzapemphera molunjika kumalo kuno; ndipo mverani Inu m'Mwamba mokhala Inumo; ndipo pamene mukumva, khululukirani. 31Ngati munthu akacimwira mnzace, ndi lumbiro likaikidwa pa iye kumlumbiritsa, ndipo akadzalumbira patsogolo pa guwa la nsembe lanu m'nyumba yino; 32mverani Inu pamenepo m'mwambamo, ndipo citani, weruzani akapolo anu, kumtsutsa woipayo, ndi kumbwezera cimo lace, ndi kulungamitsa wolungamayo kumbwezera monga cilungamo cace. 33Ndipo anthu anu Aisrayeli akawakantha adani ao cifukwa ca kucimwira Inu,

ndipo akabweranso kwa Inu, lodi kubvomereza dzina lanu, ndi kupemphera, ndi kupembedza Inu m'nyumba muno; 34pamenepo mverani Inu m'Mwambamo, ndi kukhululukira cimo la anthu anu Aisrayeli, ndi kuwabwezera ku dziko limene munapatsa makolo ao. 35Pamene kumwamba kwatsekeka, ndipo kulibe mvula cifukwa ca kucimwira Inu, nakapemphera iwo molunjika kumalo kuno, ndi kubvomereza dzina lanu, ndi kutembenuka kusiya zoipa zao, pakuwasautsa Inu; 36pamenepo mverani Inu m'Mwamba, ndi kukhululukira cimo la akapolo anu, ndi la, anthu anu Aisrayeli; pakuti muwaphunzitsa njira yokoma ayenera kuyendamo, ndi kupatsa mvula pa: dziko lanu, limene munawapatsa anthu anu likhale colowa cao. 37M'dziko mukakhala odala, mukakhala mliri, mlaza, cinoni, dzombe, kapena kapuci, adani ao akawamangira misasa m'dziko la midzi yao, mukakhala mliri uti wonse, kapena nthenda; 38tsono pempho ndi pembedzero liri lonse akalipempha munthu ali yense, kapena anthu anu onse Aisrayeli, pakuzindikira munthu yense cinthenda ca mtima wa iye yekha, ndi kutambasulira manja ace ku nyumba yino; 39pamenepo mverani Inu m'Mwamba mokhala Inu, ndi kukhululukira, ndi kucita, ndi kubwezera munthu yense monga njira zace zonse, amene Inu mumdziwa mtima wace, popeza Inu, Inu nokha, mudziwa mitima ya ana onse a anthu; 40kuti aope Inu masiku onse akukhala iwowo m'dziko limene Inu munapatsa makolo ao. 41Ndiponso kunena za mlendo, wosati wa anthu anu Aisrayeli, koma wakufumira m'dziko lakutali cifukwa ca dzina lanu, 42popeza adzamva za dzina lanu lalikuru ndi dzanja lanu lamphamvu ndi mkono wanu wotambasuka; akabwera iyeyo nadzapemphera molunjika ku nyumba yino; 43mverani Inu m'Mwamba mokhala Inu, ndipo citani monga mwa zonse mlendoyo azipempha kwa Inu; kuti anthu onse a dziko lapansi adziwe dzina lanu, kuopa Inu, monga amatero anthu anu Aisrayeli, ndi kuti adziwe kuti nyumba yino ndaimangayi yachedwa dzina lanu. 44Akaturuka anthu anu kukayambana nkhondo ndi adani ao, kumene konse inu mudzawatuma, ndipo akapemphera kwa Yehova molunjika ku mudzi uno munausankha Inu, ndi ku nyumba ndamangira dzina lanu; 45pamenepo mverani Inu m'Mwamba pempho ndi pembedzero lao, ndi kulimbitsa mlandu wao. 46Akacimwira Inu, popeza palibe munthu wosacimwa, ndipo mukakwiya nao ndi kuwapereka kwa adani, kuti iwo awatenge ndende kumka nao ku dziko la adani, ngati kutali kapena kufupi, 47ndipo akakumbukila mitima yao, ali kudziko kumene anatengedwa ukapolo, nakalapa, nakapembedza inu m'dziko la iwo anawatenga ndende, ndi kuti, Tacimwa, ndipo tacita mphulupulu, tacita moipa; 48ndipo akabwerera kwa Inu ndi mtima wao wonse ndi moyo wao wonse, m'dziko la adani ao adawatenga ndendewo,

ndipo akapemphera kwa Inu molunjika ku dziko lao munapatsa makolo aolo, ku mudzi munausankha Inu, ndi kunyumba ndamangira dzina lanu; 49pamenepo mverani Inu pemphero ndi pembedzero lao m'Mwamba mokhala Inumo, ndi kulimbitsa mlandu wao, 50ndi kukhululukira anthu anu adacimwira Inu ndi mphulupulu zao zonse adaparamula nazo kwa Inu; ndipo muwacititsire cifundo iwo amene anawagwira ndende, kuti awacitire cifundo; 51pakuti awa ndi anthu anu ndithu, ndi colowa canu cimene munaturutsa m'Aigupto, m'kati mwa ng'anjo ya citsulo; 52kuti maso anu akatsegukire pembedzero la kapolo wanu ndi pembedzero la anthu anu Aisrayeli, kuwamveram'menemonseakapfuula kwa Inu. 53Popeza Inu munawapatula pa anthu onse a pa dziko lapansi akhale colowa canu, monga munanena ndi dzanja la Mose mtumiki wanu, pamene munaturutsa makolo athu m'Aigupto, Yehova Mulungu Inu.

Solomo adalitsa Aisrayeli

54Ndipo kunali kuti atatsiriza Solomo kupemphera kwa Yehova pemphero ndi pembedzero lino lonse, ananyamuka ku guwa la nsembe la Yehova pomwe analikugwada pa mabondo ace, ndi manja ace otambasulira kumwamba. 55Naimirira, nadalitsa msonkhano wonse wa Israyeli ndi mau okweza, nati, 56Wolemekezeka ndi Yehova amene anapumulitsa anthu ace Aisrayeli, monga mwa zonse analonjezazo; sanatayika mau amodzi a mau ace onse abwino, amene analankhula ndi dzanja la Mose mtumiki wace. 57Yehova Mulungu wathu akhale nafe monga umo anakhalira nao makolo athu, asatisiye kapena kutitaya; 58kuti atitembenuzire kwa iye yekha mitima yathu iyende m'njira zace zonse, ndi kusunga malamulo ace onse ndi malemba ace ndi maweruzo ace, amene anawalamulira makolo athu. 59Ndipo mau anga amenewa ndapembedzera nao pamaso pa Yehova akhale pafupi ndi Yehova Mulungu wathu usana ndi usiku, kuti alimbitse mlandu wa kapolo wace, ndi mlandu wa anthu ace Aisrayeli, mlandu wa tsiku pa tsiku lace; 60kuti anthu onse a pa dziko lapansi akadziwe kuti Yehova ndiye Mulungu, palibe wina. 61Mitima yanu ikhale yangwiro ndi Yehova Mulungu wathu, kuyenda m'malemba ace ndi kusunga malamulo ace, monga lero lino.

62Ndipo mfumu ndi anthu onse a Israyeli pamodzi naye anaphera nsembe pamaso pa Yehova. 63Ndipo Solomo anaphera nsembe yamtendere, yophera kwa Yehova ng'ombe zikwi makumi awiri mphambu ziwiri, ndi nkhosa zikwi zana limodzi mphambu makumi awiri. Momwemo mfumu ndi ana a Israyeli onse anapereka nyumbayo ya Yehova. 64Tsiku lomwelo mfumu inapatulira Mulungu pakati pace pa bwalo la ku khomo la nyumba ya Yehova; pakuti pomwepo anapereka nsembe yopsereza ndi nsembe yaufa, ndi

mafuta a nsembe zamtendere; popeza guwa la nsembe lamkuwa
linali pamaso pa Yehova lidacepa kulandira nsembe zopsereza, ndi
nsembe zaufa, ndi mafuta a nsembe zamtendere. 65Ndipo nthawi
yomweyo Solomo anacita madyerero pamaso pa Yehova Mulungu
wathu, ndi Israyeli yense pamodzi naye, msonkhano waukuru
wakuyambira polowera ku Hamati kufikira ku nyanja ya ku Aigupto,
masiku asanu ndi awiri, ndi masiku asanu ndi awiri ena, ndiwo
masiku khumi mphambu anai. 66Tsiku lacisanu ndi citatu anawauza
anthu apite; ndipo iwo anadalitsa mfumu, napita ku mahema ao
osekera ndi okondwera mtima cifukwa ca zokoma zonse Yehova
anacitira Davide mtumiki wace, ndi Israyeli anthu ace.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Mulungu aonekanso kwa Solomo

1Ndipo kunali, atatsiriza Solomo kumanga nyumba ya Yehova, ndi
nyumba ya mfumu, ndi cifuniro conse ca Solomo
anacikhumbaco, 2Yehova anaonekera kwa Solomo nthawi yaciwiri,
monga momwe adamuonekera ku Gibeoni. 3Ndipo Yehova anati
kwa iye, Ndamva pemphero lako ndi pembedzero lako
wandipembedza nalo; ndapatula nyumba imene waimangayi
kuikamo dzina langa nthawi zosatha, ndipo maso anga ndi mtima
wanga zidzakhala kumeneko masiku onse. 4Ndipo iwe
ukadzayenda pamaso panga, monga momwe Davide atate wako
anayendera ndi mtima woona ndi wolungama, kuzicita zonse
ndakulamulirazo, ndi kusunga malemba anga ndi maweruzo
anga, 5pamenepo Ine ndidzakhazikitsa cimpando ca ufumu wako
pa Israyeli nthawi yosatha, monga ndinalonjezana ndi Davide atate
wako, ndi kuti, Sadzakusowa munthu wamwamuna pa mpando
wacifumu wa Israyeli. 6Koma mukadzabwerera pang'ono pokha
osanditsata, kapena inu, kapena ana anu, osasunga malamulo
anga ndi malemba anga amene ndawaika pamaso panu;
mukadzatumikira milungu yina ndi kuilambira; 7pamenepo Ine
ndidzalikha Aisrayeli kuwacotsera m'dziko ndidawapatsali; ndipo
nyumba yino ndapatulira dzina langayi ndidzaitaya kosapenyeka;
ndipo Israyeli adzakhala ngati mwambi ndi nkhani pakati pa anthu
onse. 8Ndipo munthu yense wopitirira pa nyumba yaitali yino
adzadabwa nayo, nadzainyoza, nadzati, Yehova watero cifukwa
ninji ndi dziko lino ndi nyumba yino? 9Ndipo anthu adzayankha,
Popeza anasiya Yehova Mulungu wao amene adaturutsa makolo ao
m'dziko la Aigupto, natsata milungu yina, nailambira, naitumikira;
cifukwa cace Yehova anawagwetsera coipa conseci.

Za midzi adaimanga Saloma, ndi zomba zace

10Ndipo kunali, zitatha zaka makumi awiri m'mene Solomo
adatsiriza nyumba ziwirizo, ndizo nyumba ya Yehova ndi nyumba
ya mfumu; 11popeza Hiramu mfumu ya Turo adamthandiza Solomo
ndi mitengo yamkungudza ndi yamlombwa ndi golidi yemwe,
monga momwe iye anafuniramo, cifukwa cace mfumu Solomo
anampatsa Hiramu midzi makumi awiri m'dziko la Galileya. 12Ndipo
Hiramu anaturuka ku Turo kukaona midzi adampatsa Solomoyo,
koma siinamkomera. 13Nati, Midzi yino mwandipatsayi njotani,
mbale wanga? Naicha dzina lao, Dziko lacikole, kufikira lero
lino. 14Ndipo Hiramu adatumiza kwa mfumu matalenti a golidi zana
limodzi mphambu makumi awiri.

15Ndipo cifukwa cace ca msonkho uja anausonkhetsa mfumu
Solomo ndi cimeneci; kuti amange nyumba ya Yehova, ndi nyumba
ya iye yekha, ndi Milo, ndi linga la Yerusalemu, ndi Hazori, ndi

Megido; ndi Gezeri. 16Pakuti Farao mfumu ya Aigupto adakwera
nalanda Gezeri, nautentha ndi moto, nawapha Akanani akukhala
m'mudzimo, naupereka kwaulere kwa mwana wace mkazi wa
Solomo. 17Ndipo Solomo anamanganso Gezeri, ndi Betihoroni
wakunsi, 18ndi Balati, ndi Tadimori wa m'cipululu m'dziko
muja, 19ndi midzi yonse yosungamo zinthu zace za Solomo, ndi
midzi yosungamo magareta ace, ndi midzi yokhalamo apakavalo
ace, ndi zina ziti zonse zidakomera Solomo kuzimanga
m'Yerusalemu, ndi ku Lebano, ndi m'dziko lonse la ufumu
wace. 20Ndipo Aamori, ndi Ahiti, ndi Aperizi, ndi Ahivi, ndi Ayebusi
otsala, amene sanali a ana a Israyeli, 21ana ao amene adatsala
m'dziko, amene ana a Israyeli sanakhoza kuononga konse, Solomo
anawasenzetsa msonkho wa nchito kufikira lero. 22Koma Solomo
sanawayesa ana a Israyeli akapolo, koma iwowo anali anthu a
nkhondo, ndi anyamata ace, ndi akalonga ace, ndi akazembe ace,
ndi oyang'anira magareta ace ndi apakavalo ace. 23Ameneyo anali
akulu a akapitao oyang'anira nchito ya Solomo, mazana asanu
mphambu makumi asanu akulamulira anthu ogwira nchito
aja. 24Koma mwana wamkazi wa Farao anaturuka m'mudzi wa
Davide kukwera ku nyumba yace adammangira Solomo,
pamenepo iye anamanganso Milo. 25Ndipo caka cimodzi Solomo
anapereka katatu nsembe zopsereza ndi zamtendere, pa guwa la
nsembe limene anammangira Yehova, nafukiza zonunkhira pa
guwa la nsembe pamaso pa Yehova, atatsiriza nyumbayo.
26Ndipo mfumu Solomo anamanga zombo zambiri ku Ezioni Geberi
uli pafupi ndi Eloti, pambali pa Nyanja Yofiira, ku dziko la
Edomu. 27Ndipo, Hiramu anatuma anyamata ace m'zombozo
amarinyero ozerewera m'nyanja, pamodzi ndi anyamata a
Solomo. 28Ndipo iwo anafika ku Ofiri, natengako golidi matalenti
mazana anai mphambu makumi awiri, nafika naye kwa mfumu
Solomo.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Mfumu yaikazi ya ku Seba adzaceza kwa Solomo ku Yerusalemu

1Ndipo atamva mfumu yaikazi ya ku Seba mbiri ya Solomo
yakubukitsa dzina la Yehova, anadza kumuyesera iye ndi miyambi
yododometsa. 2Nafika ku Yerusalemu ndi ulendo wace waukulu, ndi
ngamila zakunyamula zonunkhira, ndi golidi wambiri, ndi timiyala
ta mtengo wapatali; ndipo atafika kwa Solomo anakamba naye
zonse za m'mtima mwace. 3Ndipo Solomo anamyankha miyambi
yace yonse, panalibe kanthu kobisika ndi mfumu kamene
sanamfotozera iye. 4Ndipo pamene mfumu yaikazi ya ku Seba
adaona nzeru zonse za Solomo, ndi nyumba adaimangayo, 5ndi
zakudya za pa gome lace, ndi makhalidwe a anyamata ace, ndi
maimiriridwe a atumiki ace, ndi zobvala zao, ndi otenga zikho ace,
ndi nsembe yace yopsereza imene amapereka m'nyumba ya
Yehova, anakhululuka malungo. 6Ndipo anati kwa mfumu, idali
yoonadi mbiri ija ndinaimva ine ku dziko langa ya macitidwe anu
ndi nzeru zanu. 7Koma sindinakhulupira mau amenewo mpaka
ndafika ine kuno, ndaona ndi maso anga; ndipo taonani,
anangondiuza dera lina lokha; nzeru zanu ndi zokoma zanu zakula
pa mbiri ndinaimvayo. 8Odala anthu anu, odala anyamata anu
akukhala nthawi zonse pamaso panu, akumvaimva nzeru
yanu. 9Wolemekezeka Yehova Mulungu wanu amene anakondwera
nanu, kukuikani pa mpando wacifumu wa Israyeli; popeza Yehova
anakonda Israyeli nthawi yosatha, cifukwa cace anakulongani inu
ufumu, kuti mucite ciweruzo ndi cilungamo. 10Ndipo mkaziyo
ananinkha mfumu matalenti a golidi zana limodzi mphambu
makumi awiri, ndi zonunkhira zaunyinji, ndi timiyala ta mtengo
wapatali; sunafikanso unyinji wotero wa zonunkhira wolingana ndi
uja mfumu yaikazi inapereka kwa mfumu Solomo. 11Ndipo zombe
za Hiramu zotengera golidi ku Ofiri zinatenganso ku Ofiri mitengo
yambiri yambawa, ndi timiyala ta mtengo wapatali. 12Ndipo
mfumu inasema mitengo yambawayo, ikhale mizati ya nyumba ya
Yehova, ndi ya nyumba ya mfumu; ndiponso azeze ndi zisakasa za
oyimbawo; siinafika kapena kuonekanso mpaka lero mitengo
yotero yambawa. 13Ndipo mfumu Solomo ananinkha mfumu
yaikazi ya ku Seba cifuniro cace conse anacipempha iye,
osawerenga cimene Solomo anamninkha mwa ufulu waceo
Momwemo iye anabwerera namukanso ku dziko lace, iyeyo ndi
anyamata ace.

Cuma ndi ukulu wa Solomo

14Tsono kulemera kwace kwa golidi anafika kwa Solomo caka
cimodzi kunali matalenti mazana asanu ndi limodzi mphambu
makumi asanu ndi limodzi kudza asanu ndi liimodzi a

golidi, 15osawerenganso winayo wa anthu a malonda
oyendayenda, ndi wa amalonda ena, ndi wa mafumu onse a Arabu,
ndi wa akazembe onse a madera. 16Ndipo mfumu Solomo
anapanga zikopa mazana awiri zagolidi wonsansantha, cikopa
cimodzi cinapangidwa ndi masekeli mazana asanu ndi
limodzi. 17Ndi malihawo mazana atatu a golidi wonsansantha,
libawo limodzi linapangidwa ndi miyeso itatu ya golidi; ndipo
mfumu inazisungira zonse m'nyumba yochedwa Nkhalango ya
Lebano. 18Ndipo mfumu inapanga mpando waukulu wacifumu
waminyanga, naukuta ndi golidi woyengetsa. 19Mpandowo
wacifumu unali ndi makwerero asanu ndi limodzi, ndi pamwamba
pa mpando wacifumu panali pozungulira kumbuyoko, ndipo munali
ngati manja m'mbali zonse ziwiri za pokhalirapo, naimika mikango
iwiri m'mbali mwa manjawo. 20Ndipo anaimikamikango khumi ndi
iwiri mbali yina ndi yina, pa makwerero asanu ndi limodzi aja;
m'dziko liri lonse tina simunapangidwa wotere. 21Ndipo zikho
zomwera zonse za mfumu Solomo zinali zagolidi, ndi zotengera
zonse za nyumba yochedwa Nkhalango ya Lebano zinali zagolidi
yekha yekha, panalibe zasiliva, pakuti siliva ana ngoyesedwa
opanda pace masiku onse a Solomo. 22Popeza mfumu inali nazo
panyanja zombo za ku Tarisi, pamodzi ndi zombo za Hiramu;
zombo za ku Tarisi zinafika, kamodzi zitapita zaka zitatu, ziri nazo
golidi, ndi siliva, ndi minyanga, ndi apusi, ndi mbalame za zitsukwa
zazitali za maanga maanga. 23Ndipo mfumu Solomo anawaposa
mafumu onse a dziko lapansi pa cuma ndi nzeru. 24Ndipo anthu
onse a pa dziko anafuna nkhope ya Solomo, kudzamva nzeru zace
zimene Mulungu analonga m'mtima mwace. 25Ndipo akafika
munthu yense ndi mtulo wace, zotengera zasiliva, ndi zotengera
zagolidi, ndi zobvala, ndi zida, ndi zonunkhira, ndi akavalo, ndi
nyuru; momwemo caka ndi caka. 26Ndipo Solomo anasonkhanitsa,
magareta ndi apakavalo; anali nao magareta cikwi cimodzi
mphambu, mazana anai, ndi apakavalo zikwi khumi mphambu
ziwiri, nawasungira m'midzi yosungamo magareta, ndi kwamfumu
m'Yerusalemu. 27Ndipo mfumu inacurukitsa siliva ngati miyala
m'Yerusalemu, ndi mitengo yamikungudza anailinganiza ndi
mikuyu ya m'madambo. 28Ndipo akavalo a Solomo anacokera ku
Aigupto; anthu a malonda a mfumu anawagula magulu magulu,
gulu liri lonse mtengo wace. 29Ndipo gareta limodzi linacokera
kuturuka m'Aigupto mtengo wace masekeli a siliva mazana asanu
ndi limodzi, ndi kavalo mtengo wace masekeli zana limodzi
mphambu makumi asanu; momwemonso iwo anawagulira mafumu
onse a Ahiti ndi mafumu a Aramu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Solomo adzipereka kupembedza mafano; Mulungu aipidwa naye

1Ndipo mfumu Solomo anakonda akazi ambiri acilendo, pamodzi
ndi mwana wamkazi wa Farao, akazi a ku Moabu, ndi a ku Amoni,
ndi a ku Edomu, ndi a ku Zidoni, ndi Ahiti; 2a mitundu ija Yehova
adanena ndi ana a Israyeli za iwo, kuti, Inu musakalowa kwa iwo,
ndipo iwo asadzalowe kwa inu; zedi adzatembenuza mitima yanu
kutsata milungu yao; amenewo Solomo anawaumirira
kuwakonda. 3Ndipo anali nao akazi mazana asanu ndi awiri, ana
akazi a mafumu, ndi akazi acabe mazana atatu; ndipo akazi ace
anapambutsa mtima wace. 4Ndipo kunali, atakalamba Solomo,
akazi ace anapambutsa mtima wace atsate milungu yina; ndipo
mtima wace sunakhala wangwiro ndi Yehova Mulungu wace monga
mtima wa Davide atate wace. 5Tsono Solomo anatsata Asitoreti
fano la anthu a Zidoni, ndi Milikomu fano lonyansitsa la
Aamoni. 6Ndipo Solomo anacita coipa pamaso pa Yehova, osatsata
Yehova ndi mtima wonse monga Davide atate wace. 7Pamenepo
Salomo anamangira Kemosi fano lonyansitsa la Amoabu ndi Moleki
fano lonyansitsa la ana a Amoni misanje, pa phiri liri patsogolo pa
Yerusalemu. 8Ndipo momwemo anacitiranso akazi ace onse
acilendo, amene amafukizira naphera nsembe mafano ao.
9Ndipo Yehova anakwiya ndi Solomo, pokhala mtima wace
unapambuka kwa Yehova Mulungu wa Israyeli, amene
adamuonekera kawiri, 10namlamulira za cinthu comweci, kuti
asatsate milungu yina; koma iye sanasunga cimene Yehova
anacilamula. 11Cifukwa cace Yehova ananena ndi Solomo, Popeza
cinthu ici cacitika ndi iwe, ndipo sunasunga cipangano canga ndi
malemba anga amene ndinakulamulira, zedi, ndidzakung'ambira
ufumu ndi kuupatsa mnyamata wako. 12Koma m'masiku ako
sindidzatero cifukwa ca Davide atate wako, koma
ndidzaung'ambira m'manja mwa mwana wako; 13komatu
sindidzacotsa ufumu wonsewo; pfuko limodzi ndidzapatsa mwana
wako, cifukwa ca Davide mtumiki wanga, ndi cifukwa ca
Yerusalemu amene ndinamsankha.

Mulungu amuutsira Solomo adani

14Ndipo Yehova anamuutsira Solomo mdani, ndiye Hadadi M-
edomu; iyeyo anali wa mbumba ya mfumu ya ku Edomu. 15Pakuti
pamene Davide adali m'Edomu, ndipo Yoabu kazembe wa nkhondo
adanka kukaika akufawo, atapha amuna onse m'Edomu; 16pakuti
Yoabu ndi Aisrayeli onse anakhalako miyezi isanu ndi umodzi,
mpaka atawapha amuna onse m'Edomu; 17Hadadi uja anathawa,
iyeyo ndi a ku Edomu ena, akapolo a atate wace pamodzi naye,
kumka ku Aigupto, Hadadiyo akali mwana. 18Ndipo anacoka ku

Midyani nafika ku Parani, natenga anthu a ku Parani pamodzi nao, nafika ku Aigupto kwa Farao mfumu ya Aigupto, ameneyo anampatsa nyumba, namnenera zakudya, nampatsako dziko. 19Ndipo Farao anamkomera mtima ndithu Hadadiyo, nampatsa mkazi ndiye mbale wa mkazi wace, mbale wace wa Takipenesi mkazi wamkulu wa mfumu. 20Ndipo mbale wa Takipenesi anamuonera Genubati mwana wace, ameneyo Takipenesi anamletsera kuyamwa m'nyumba ya Farao, ndipo Genubati anakhala m'banja la Farao pamodzi ndi ana amuna a Farao. 21Ndipo atamva Hadadi ku Aigupto kuti Davide anagona ndi makolo ace, ndi kuti Yoabu kazembe wa nkhondo adafanso, Hadadi ananena ndi Farao, Mundilole ndimuke ku dziko la kwathu. 22Tsono Farao anati kwa iye, Koma cikusowa iwe nciani kwa ine, kuti ufuna kumuka ku dziko la kwanu? Nayankha iye, Palibe kanthu, koma mundilole ndimuke ndithu.
23Ndipo Mulungu anamuutsira mdani wina, ndiye Rezoni mwana wa Eliyada, amene adathawa mbuye wace Hadadezeri mfumu ya ku Zoba. 24Iye nasonkhanitsa anthu, nakhala kazembe wa nkhondo, muja Davide anawapha a ku Zobawo, napita ku Damasiko, hakhala komweko, nakhala mfumu ya ku Damasiko. 25Ndipo iye anali mdani wa Israyeli masiku onse a Solomo, kuonjezerapo coipa anacicita Hadadi, naipidwa nao Aisrayeli, nakhala mfumu ya ku Aramu.

Mneneri Ahiya agawira Yerobiamu ufumuwo

26Ndipo Yerobiamu mwana wa Nebati M-efrati wa ku Zereda mnyamata wa Solomo, dzina la amace ndiye Zeruwa, mkazi wamasiye, iyenso anakweza dzanja lace pa mfumu. 27Ndipo cifukwa cakukweza iye dzanja lace pa mfumu ndi cimeneci: Solomo anamanga Milo, namanganso pogumuka pa linga la mudzi wa Davide atate wace. 28Ndipo munthu ameneyo Yerobiamu anali ngwazi; ndipo pamene Solomo anamuona mnyamatayo kuti ngwacangu, anamuika akhale woyang'anira wa nchito yonse ya nyumba ya Yosefe. 29Ndipo kunali nthawi yomweyo kuti Yerobiamu anaturuka m'Yerusalemu, ndipo mneneri Ahiya wa ku Silo anampeza m'njira; tsono iyeyo anabvaliratu cobvala catsopano, ndipo iwo awiri anali okha kuthengo. 30Ndipo Ahiyayo anagwira cobvala cace catsopano, nacing'amba khumi ndi pawiri. 31Nati kwa Yerobiamu, Takwaya magawo khumi; popeza atero Yehova Mulungu wa Israyeli, Taona ndidzaung'amba ufumu m'dzanja la Solomo ndi kukupatsa iwe mafuko khumi. 32Koma iye adzakhala nalo pfuko limodzi, cifukwa ca Davide mtumiki wanga, ndi ca Yerusalemu, mudzi umene ndinausankha m'mafuko onse a Israyeli. 33Nditero popeza iwo anandisiya, napembedza Asitoreti mulungu wa Azidoni, ndi Kemosi mulungu wa Amoabu, ndi Milikomu mulungu wa ana a

Amoni, osayenda m'njira zanga, kucita cimene ciyenera pamaso
panga, ndi kusunga malemba anga ndi maweruzo anga, monga
umo anatero Davide atate wace. 34Koma sindidzalanda ufumu
wonse m'dzanja lace, koma ndidzamkhalitsa mfumu masiku ace
onse, cifukwa ca Davide mtumiki wanga amene uja ndinamsankha,
cifukwa kuti anasunga malamulo anga ndi malemba anga. 35Koma
ndidzalanda ufumu m'dzanja la mwana wace, ndi kupatsa iwe
mafuko khumi amene. 36Ndipo ndidzamninkha mwana wace pfuko
limodzi, kuti Davide mtumiki wanga akhale cikhalire ndi nyali
pamaso panga m'Yerusalemu, mudzi umene ndinadzisankhira
kuikapo dzina langa. 37Ndipo ndidzakutenga iwe, ndipo udzacita
ufumu monga umo ukhumbira moyo wako, nudzakhala mfumu ya
Israyeli. 38Ndipo kudzakhala kuti ukadzamvera iwe zonse
ndikulamulirazo, nukadzayenda m'njira zanga ndi kucita cilungamo
pamaso panga, kusunga malemba anga ndi malamulo anga,
monga anatero Davide mtumiki wanga pamenepo Ine ndidzakhala
ndi iwe, ndidzakumangira ndi kukukhazikitsira nyumba, monga
nelinammangira Davide, ndipo ndidzakupatsa iwe Israyeli. 39Ndipo
cifukwa ca ici nelidzazunza mbumba ya Davide, koma si masiku
onse ai. 40Cifukwa cace Solomo anafuna kupha Yerobiamu, ndipo
Yerobiamu anathawira ku Aigupto kwa Sisaki mfumu ya Aigupto,
nakhala m'Aigupto kufikira imfa ya Solomo.

Imfa ya Solomo

41Ndipo macitidwe otsiriza a Solomo, ndi nchito zace zonse
anazicita, ndi nzeru zace, kodi sizilembedwa zimenezo m'buku la
madtidwe a Solomo? 42Ndipo masiku amene Solomo anakhala
mfumu ya Aisrayeli onse m'Yerusalemu anali zaka makumi
anai. 43Ndipo Solomo anagona ndi makolo ace, naikidwa m'mudzi
wa Davide atate wace; ndipo Rehabiamu mwana wace anakhala
mfumu m'malo mwace.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Rehabiamu sam vera uphungu wa akuru

1Ndipo Rehabiamu anamka ku Sekemu, popeza Aisrayeli onse
anadza ku Sekemu kumlonga ufumu. 2Ndipo kunali kuti Yerobiamu
mwana wa Nebati anacimva akali m'Aigupto, kumene anathawira
kucokera ku maso a Solomo mfumu, pakuti Yerobiamu anakhala ku
Aigupto. 3Ndipo anatuma akukamuitana. Ndipo Yerobiamu ndi
msonkhano wonse wa Israyeli anadza, nalankhulana ndi
Rehabiamu, nati, 4Atate wa nu analemeretsa gori lathu, ndipo inu
tsono pepuzaniko nchito zosautsa za atate wanu, ndi gori lolemera
lace limene anatisenza, ndipo tidzakutumikirani. 5Ndipo iye anati
kwa iwo, Bamukani, mukagone masiku atatu, pamenepo
mukabwera kwa ine. Ndipo anthu anamuka. 6Ndipo mfumu
Rehabiamu anafunsira kwa mandoda, amene anaimirira pamaso
pa Solomo atate wace, akali moyoiyeyo, nati, Inu mundipangire
bwanji kuti ndiyankhe anthu awa? 7Ndipo iwo anamuuza kuti,
Mukakhala inu mtumiki wa anthu awa lero, ndi kuwatumikira ndi
kuwayankha ndi kukamba nao mau okoma, tsono iwo adzakhala
cikhalire atumiki anu. 8Koma iye analeka uphungu wa mandodawo,
umene anampangirawo, nakafunsira kwa acinyamata anzace
oimirira pamaso pace, 9nati kwa lwo, Kodi inu mundipangire bwanji
kuti tiyankhe anthu awa anandiuza ine, kuti, Mupepuze gori limene
atate wanu anatisenza ife? 10Ndipo acinyamata anzace ananena
naye, Dati, Mzitero ndi anthu awa adalankhula nanu, nati, Atate
wanu analemeretsa gori lathu, koma inu mutipepuzire limenelo;
mzitero nao, Kanense wanga adzaposa m'cuuno mwa atate
wanga. 11Ndipo tsopano, popeza atate wanga anakusenzani gori
lolemera, ine ndidzaonjezerapo pa gori lanu, atate wanga
anakukwapulani ndi zikoti, koma ine ndidzakukwapulani ndi
zinkhanira. 12Ndipo Yerobiamu ndi anthu onse anabwera kwa
Rehabiamu tsiku lacitatu monga momwe anawauzira mfumu, nati,
Bweraninso kwa ine tsiku lacitatu. 13Ndipo mfumu inayankha anthu
mau okalipa, naleka uphungu anampangira
mandodawo, 14nalankhula nao monga mwa uphungu wa
acinyamata, nati, Atate wanga analemeretsa gori lanu, koma ine
ndidzaonjezerapo pa gori lanu; atate wanga anakukwapulani ndi
zikoti, koma ine ndidzakukwapulani ndi zinkhanira, 15Potero mfumu
siinamvera anthuwo, pakuti kusintha uku kunacokera kwa Yehova,
kuti akhazikitse mau ace amene Yehova ananenetsa Abiya wa ku
Silo kwa Yerobiamu mwana wa Nebati. 16Ndipo pakuona Aisrayeli
onse kuti mfumu siinawamvera iwo, anthuwo anayankha mfumu,
Tiri naye ciani Davide? inde tiribe colowa m'mwana wa Jese; tiyeni
kwathu Aisrayeli inu; yang'aniranitu, nyumba yako, Davide.
Momwemo Aisrayeli anacoka kumka ku mahema ao. 17Kama ana

aja a Israyeli akukhala m'midzi ya Yuda, Rehabiamu anakhalabe
mfumu yao. 18Pamenepo mfumu Rehabiamu anatuma Adoramu
wamsonkho, ndipo Aisrayeli onse anamponya miyala, nafa. Ndipo
mfumu Rehabiamu anafulumira kulowa m'gareta wace kuthawira
ku Yerusalemu. 19Motero Aisrayeli anapandukana ndi nyumba ya
Davide kufikira lero. 20Ndipo kunali, atamva Aisrayeli onse kuti
Yerobiamu wabweranso, anatuma kumuitanira iye kumsonkhano,
namlonga iye mfumu ya Aisrayeli onse; palibe munthu anatsata
nyumba ya Davide koma pfuko lokha la Yuda.
21Ndipo Rehabiamu anafika ku Yerusalemu, nasonkhanitsa nyumba
yonse ya Yuda, ndi pfuko la Benjamini, ankhondo osankhika zikwi
zana limodzi mphambu makumi asanu ndi atatu, kuyambana nayo
nyumba ya Israyeli, kubwezanso ufumu kwa Rehabiamu mwana wa
Solomo. 22Ndipo mau a Mulungu anafika kwa Semaya mneneri wa
Mulungu, nati, 23Lankhula kwa Rehabiamu mwana wa Solomo
mfumu ya Yuda, ndi kwa nyumba yonse ya Yuda, ndi Benjamini, ndi
kwa anthu otsalawo, nuti, 24Yehova atero, Musamuka, ndipo
musakayambana ndi abale anu ana a Israyeli, bwererani yense
kunyumba kwace; popeza cinthuci cacokera kwa Ine. Ndipo iwo
anamvera mau a Yehova, natembenuka, nabwerera monga mwa
mau a Yehova.

Kupembedza mafano kwa Yerobiamu

25Ndipo Yerobiamu anamanga Sekemu m'mapiri a Efraimu,
nakhalamo, naturukamo, namanga Penueli. 26Ndipo Yerobiamu
ananena m'mtima mwace, Ufumuwu udzabwereranso ku nyumba
ya Davide. 27Anthu awa akamakwera kukapereka nsembe
m'nyumba ya Yehova m'Yerusalemu, pamenepo mitima ya anthu
awa idzatembenukiranso kwa mbuye wao, kwa Rehabiamu mfumu
ya Yuda; ndipo adzandipha, nadzabweranso kwa Rehabiamu
mfumu ya Yuda. 28Potero mfumu inakhala upo, napanga ana a
ng'ombe awiri agolidi, nati kwa iwo, Kukulemetsani kukwera ku
Yerusalemu; tapenyani Aisrayeli inu milungu yanu imene
inakuturutsani m'dziko la Aigupto. 29Ndipo anaimika mmodzi ku
Beteli, naimika wina ku Dani. 30Koma cinthu ici cinasanduka:
chimo, ndipo anthu anamka ku mmodziyo wa ku Dani. 31Iye
namanga nyumba za m'misanje, nalonga anthu acabe akhale
ansembe, osati ana a Levi ai. 32Ndipo Yerobiamu anaika madyerero
mwezi wacisanu ndi citatu, tsiku lakhumi ndi cisanu la mwezi
olingana ndi madyerero aja a ku Yuda, napereka nsembe pa guwa
la nsembe; anatero m'Beteli, nawaphera nsembe ana a ng'ombe
aja anawapanga, naika m'Beteli ansembe a misanje imene
anaimanga. 33Ndipo anapereka nsembe pa guwa la nsembe
analimanga m'Beteli, tsiku lakhumi ndi cisanu la mwezi wacisanu
ndi citatu, m'mwezi umene anaulingirira m'mtima mwa iye yekha,

nawaikira ana a Israyeli madyerero, napereka nsembe pa guwa la nsembe, nafukiza zonunkhira.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Mneneri adzudzula Yerobiamu

1Ndipo onani, munthu wa Mulungu anacokera ku Yuda mwa mau a
Yehova nadza ku Beteli; ndipo Yerobiamu anali kuimirira m'mbali
mwa guwa la nsembe kufukiza zonunkhira. 2Ndipo iye anapfuula
mwa mau a Yehova kutemberera guwa la nsembe, nati, Guwa la
nsembe, guwa la nsembe, atero Yehova, Taona mwana adzabadwa
m'nyumba ya Davide, dzina lace ndi Yosiya, adzaphera pa iwe
ngati nsembe anthu ansembe a misanje, amene alikufukiza
zonunkhira pa iwe, nadzatentha pa iwe mafupa a anthu. 3Ndipo iye
anapatsa cizindikilo tsiku lomwelo, nari, Cizindikilo cimene Yehova
ananena ndi ici, Taonani guwali la nsembe lidzang'ambika, ndi
phulusa liri pa ilo lidzatayika. 4Ndipo kunacitika, pa kumva mfumu
mau a munthu wa Mulungu amene anawapfuula, kutemberera
guwa la nsembe m'Beteli, Yerobiamu anatansa dzanja lace ali ku
guwalo, nati, Mgwireni iye. Ndipo dzanja lace analitansira kwa iye
linauma, kuti sanatha kulipfunyatitsanso. 5Ndiponso guwalo
linang'ambika, ndi phulusa la pa guwalo linatayika, monga mwa
cizindikilo cimene munthu wa Mulungu anapatsa mwa mau a
Mulungu. 6Ndipo mfumu inayankha niti kwa munthu wa Mulungu,
Undipembedzere Yehova Mulungu wako, nundipempherere, kuti
dzanja langa libwerenso kwa ine. Ndipo munthuyo wa Mulungu
anapembedza Yehova, ndipo dzanja la mfumu linabwezedwa kwa
iye momwemo mwa kale. 7Mfumu niti kwa munthu wa Mulungu,
Tiye kwathu, ukapumule, ndikupatse mphatso. 8Ndipo munthu wa
Mulungu ananena ndi mfumu, Mungakhale mundigawira pakati ndi
pakati nyumba yanu, sindilowa kwa inu, kapena kudya mkate,
kapena kumwa madzi kuno. 9Pakuti potero ndinalamulidwa ndi
mau a Yehova, ndi kuti, Usakadye mkate, kapena kumwa madzi,
kapena kubwerera njira yomweyo unadzerayo. 10Tsono iye
anayenda njira yina osabwerera njira yomweyo anaidzera pakudza
ku Beteli.

Mneneri wosamverayo aphedwa ndi mkango

11Ndipo ku Beteli kunakhala mneneri wokalamba, ndipo mwana
wace wina anadzamfotokozera macitidwe onse anawacita munthu
wa Mulunguyo tsiku lomwelo m'Beteli ndi mau ace anawanena ndi
mfumu; inde omwe aja iwo anamfotokozera atate wao. 12Ndipo
atate wao anati kwa iwo, Wapitira njira yiti? popeza ana ace
adaona njira analowera munthu wa Mulungu anacokera ku
Yudayo. 13Nanena ndi ana ace, Ndimangireni mbereko pa buru.
Namangira iwo mbereko pa buru, naberekekapo iye. 14Natsata
munthu wa Mulungu, nampeza ali, tsonga patsinde pa mtengo
wathundu, nanena naye, Kodi ndiwe munthu wa Mulungu amene
uja anacokera ku Yuda? Nati, Ndine amene. 15Tsono ananena naye,

Tiye kwathu, ukadye mkate. 16Nan iye, Sindingabwerere nawe
kukalowa kwanu, kapena kudya mkate, kapena kumwa nawe
madzi pano; 17pakuti mau a Yehova anadza kwa ine, nati Usakadye
mkate, kapena kumwa madzi kumeneko, kapena kubwerera njira
yomweyo unadzerayo. 18Ndipo anati kwa iye, Inenso ndine
mneneri wonga iwe, ndipo mthenga analankhula ndi ine mwa mau
a Yehova, nati, Kambwezere kwanu, kuti akadye mkate, namwe
madzi. Koma anamnamiza. 19Tsono anabwerera naye, nakadya
kwao, namwa madzi. 20Ndipo kunacitika iwo ali cikhalire pagome,
mau a Yehova anadza kwa mneneri amene
anambwezayo, 21napfuula iye kwa munthu uja wa Mulungu
anacokera ku Yudayo, nati, Atero Yehova, Pokhala sunamvera mau
a pakamwa pa Yehova, osasunga lamulo lija Yehova Mulungu wako
anakulamulira, 22koma unabwerera nudya mkate, ndi kumwa
madzi paja pomwe iye anakuuza, Usakadye mkate, kapena kumwa
madzi, mtembo wako tsono sudzaikidwa ku manda a atate
ako. 23Ndipo kunacitika, atadya iye mkate, ndi kumwa madzi,
anammangira mbereko pa buru mneneri amene
anambwezayo. 24Ndipo atacoka iye, mkango unakomana naye
panjira, numupha, ndipo mtembo wace unagwera m'njiramo, buru
naima pafupi, mkangonso unaima pafupi ndi mtembo. 25Ndipo
onani, anthu anapitapo naona mtembo wogwera m'njiramo, ndi
mkango uli ciimire pafupi ndi mtembo, nadzanena m'mudzi
m'mene munakhala mneneri wokalamba uja. 26Ndipo mneneri
amene uja anambweza panjirayo atamva, anati, Ndiye munthu uja
wa Mulungu amene sanamvera mau a Yehova; cifukwa cace
Yehova wampereka kwa mkango, numkadzula numupha, monga
mwa mau a Yehova analankhula nayewo. 27Iye nanena ndi ana
ace, nati, Ndimangireni mbereko pa buru. Namangira
mbereko. 28Namuka iye, napeza mtembo wace wogwera m'njira,
ndi buru ndi mkango ziti ciimire pafupi ndi mtembo. Mkango
udalibe kudya mtembo, kapena kukadzula buru. 29Ndipo mneneri
ananvamula mtembo wa munthu wa Mulunguyo, nausenza pa
buru, nabwera nao, nalowa m'mudzi mneneri wokalamba kumlira
ndi kumuika. 30Ndipo mtembo wace anauika m'manda a iye mwini,
namlira iwo maliro, nati, Mayo, mbale wanga! 31Ndipo kunacitika,
atamuika iye, ananena ndi ana ace, nati, Nkadzamwalira ine
mudzandiike ine m'manda momwemo mwaikidwa munthu wa
Mulunguyo, ikani mafupa anga pafupi ndi mafupa ace. 32Popeza
mau aja anawapfuula mwa mau a Yehova kutemberera guwa la
nsembe la ku Beteli, ndi kutemberera nyumba zonse za misanje iri
m'midzi ya ku Samariya, adzacitika ndithu.
33Pambuyo pa ici Yerobiamu sanabwerera pa njira yace yoipa,
koma analonganso anthu acabe akhale ansembe a misanje,

yensewakufuna yemweyu anampatula akhale wansembe wa misanje, 34Ndimo umu munali chimo la nyumba ya Yerobiamu, limene linaidula ndi kuiononga pa dziko lapansi.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Ahiya aneneratu kugwa kwa Yerobiamu

1Nthawi yomweyo Abiya mwana wa Yerobiamu anadwala. 2Ndipo
Yerobiamu ananena ndi mkazi wace, Unyamuke, nudzizimbaitse,
ungadziwike kuti ndiwe mkazi wa Yerobiamu, nupite ku Silo; taona,
kumeneko kuli Ahiya mneneri uja anandiuza ine ndidzakhala
mfumu ya anthu awa. 3Nupite nayo mikate khumi, ndi timitanda,
ndi cigulu ca uci, numuke kwa iye; adzakuuza m'mene umo
akhalire mwanayo. 4Natero mkazi wa Yerobiamu, nanyamuka
namka ku Silo, nalowa m'nyumba ya Ahiya. Koma Ahiya sanatha
kupenya, popeza maso ace anali tong'o, cifukwa ca ukalamba
wace. 5Ndipo Yehova ananena ndi Ahiya, Taona, mkazi wa
Yerobiamu akudza kukufunsa za mwana wace, popeza adwala;
udzanena naye mwakuti mwakuti; popeza kudzakhala pakulowa
iye adzadzizimbaitsa. 6Ndipo kunacitika, pamene Ahiya anamva
mgugu wa mapazi ace alinkulowa pakhomo, anati, Lowa mkazi iwe
wa Yerobiamu, wadzizimbaitsiranji? pakuti ine ndatumidwa kwa iwe
ndi mau olasa. 7Kauze Yerobiamu, Atero Yehova Mulungu wa
Israyeli, Ndingakhale ndinakukulitsa pakati pa anthu, ndi
kukukhalitsa mfumu ya anthu anga Aisrayeli, 8ndipo ndinalanda
nyumba ya Davide ufumu, ndi kuupereka kwa iwe, koma
sunafanana ndi Davide mtumiki wanga uja, amene anasunga
malamulo anga, nanditsata ndi mtima wace wonse kucita zolunjika
zokha zokha pamaso panga; 9koma wacimwa koposa onse akale,
nukadzipangira milungu yina ndi mafano yoyenga kundikwiyitsa,
nunditaya Ine kumbuyo kwako; 10cifukwa cace, taona, ndidzafikitsa
coipa pa nyumba ya Yerobiamu, ndi kugurula mwana wamwamuna
yense wa Yerobiamu womangika ndi womasuka m'Israyeli, ndipo
ndidzacotsa psiti nyumba yonse ya Yerobiamu, monga munthu
acotsa ndowe kufikira idatha yonse. 11Agaru adzadya ali yense wa
Yerobiamu wakufa m'mudzi; ndi mbalame za m'mlengalenga
zidzadya yense wakufera kuthengo; popeza wanena ndi
Yehova. 12Tanyamuka tsono, numuke kwanu; pakulowa mapazi ako
m'mudzi mwanayo adzatsirizika. 13Ndipo Aisrayeli onse adzamlira,
nadzamuika, popeza iye yekha wa ana a Yerobiamu adzalowa
m'manda; pakuti mwa iye mwapezedwa cokoma ca kwa Yehova
Mulungu wa Israyeli m'nyumba ya Yerobiamu. 14Ndiponso Yehova
adzadziukitsira mfumu ya Israyeli, idzaononga nyumba ya
Yerobiamu tsiku lomwelo; nciani ngakhale tsopano apa? 15Popeza
Yehova adzawakantha Aisrayeli monga bango ligwedezeka ndi
madzi, nadzazula Aisrayeli m'dziko lino labwino analipatsa makolo
ao, nadzawamwazira ku tsidya lija la Firate, popeza iwo anapanga
zifanizo zao zokwiyitsa Yehova. 16Ndipo adzai pereka Aisrayeli
cifukwa ca macimo a Yerobiamu anacimwawo, nacimwitsa nao

Aisrayeli. 17Ndipo mkazi wa Yerobiamu ananyamuka nacoka, nafika
ku Tiriza; ndipo polowa iye pa khomo la nyumba yace anatsirizika
mwanayo. 18Ndipo anamuika, namlira Aisrayeli, monga mwa mau
a Yehova anawalankhula pa dzanja la mtumiki wace Ahiya
mneneri. 19Ndipo macitidwe ena a Yerobiamu m'mene umo
anacitira nkhondo, ndi m'mene umo anacitira ufumu, taona,
analembedwa m'buku la macitidwe a mafumu a Israyeli. 20Ndipo
masiku akukhala Yerobiamu mfumu anali zaka makumi awiri
mphambu ziwiri, nagona iye kwa makolo ace, nalowa ufumu
m'malo mwace Nadabu mwana wace.

Yuda aipsidwa mwa Rehabiamu

21Ndipo Rehabiamu mwana wa Solomo anali mfumu ya dziko la
Yuda. Rehabiamu anali wa zaka makumi anai mphambu cimodzi
polowa ufumu wace, nakhala mfumu zaka khumi mphambu zisanu
ndi ziwiri m'Yerusalemu, m'mudzi m'mene Yehova adausankha
m'mafuko onse a Israyeli kukhazikamo dzina lace. Ndipo dzina la
amace linali Naama M-amoni. 22Ndipo Ayuda anacita zoipa pamaso
pa Yehova, namcititsa nsanje ndi zoipa zao anazicitazo, zakuposa
zija adazicita makolo ao, 23Pakuti anadzimangiranso misanje, ndi
zoimiritsa, ndi zifanizo, pa citunda conse cacitali, ndi patsinde pa
mtengo wogudira uli wonse; 24panalinso anyamata ocitirana dama
m'dzikomo; iwo amacita monga mwa zonyansitsa za amitundu,
amene Yehova anapitikitsa pamaso pa ana a Israyeli. 25Ndipo
kunacitika, Rebabiamu atakhala mfumu zaka zisanu, Sisaki mfumu
ya Aigupto anakwera ndi nkhondo ku Yerusalemu, 26nacotsa cuma
ca m'nyumba ya Yehova, ndi cuma ca m'nyumba ya mfumu; inde
anacotsa conseco, nacotsanso zikopa zagolidi zonse adazipanga
Solomo. 27Ndipo mfumu Rehabiamu anapanga m'malo mwa izo
zikopa zina zamkuwa, nazipereka m'manja a akapitao a olindirira,
akusunga pakhomo pa nyumba ya mfumu. 28Ndipo kunacitika,
pakulowa mfumu m'nyumba ya Yehova, olindirira aja
anazinyamula, nabweranso nazo ku cipinda ca
olindirirawo. 29Tsono, macitidwe ace ena a Rehabiamu, ndi zonse
anazicita, kodi sizilembedwa m'buku la macitidwe a mafumu a
Yuda? 30Ndipo panali nkhondo pakati pa Rehabiamu ndi Yerobiamu
masiku ao onse. 31Nagona Rehabiamu ndi makolo ace, naikidwa
kwa makolo ace m'mudzi wa Davide. Ndipo dzina la amace linali
Naama M-amoni, nalowa ufumu m'malo mwace Abiya mwana
wace.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Abiya atsata zoipa za atate wace Rehabiamu

1Ndipo caka cakhumi mphambu zisanu ndi zitatu ca mfumu
Yerobiamu mwana wa Nebati, Abiya analowa ufumu wa
Yuda. 2Anakhala mfumu zaka zitatu m'Yerusalemu, ndipo dzina la
amace linali Maaka mwana wa Abisalomu. 3Nayenda iye m'zoipa
zonse za atate wace, zimene iye adacita asanalowe ufumu
Abiyayo; ndipo mtima wace sunali wangwiro ndi Yehova Mulungu
wace monga mtima wa Davide kholo lace. 4Koma cifukwa ca
Davideyo Yehova Mulungu wace anampatsa nyali m'Yerusalemu,
kumuikira mwana wace pambuyo pace, ndi kukhazikitsa
Yerusalemu; 5cifukwa kuti Davide adacita colungama pamaso pa
Yehova, osapambuka masiku ace onse pa zinthu zonse
adamlamulira iye, koma cokhaco cija ca Uriya Mhiti. 6Ndipo panali
nkhondo pakati pa Abiya ndi Yerobiamu masiku onse a moyo
wace. 7Ndipo macitidwe ace ena a Abiya, ndi zonse anazicita, kodi
sizilembedwa m'buku la macitidwe a mafumu a Yuda? Ndipo panali
nkhondo pakati pa Abiya ndi Yerobiamu. 8Nagona Abiya ndi makolo
ace, namuika anthu m'mudzi wa Davide; Asa mwana wace nalowa
ufumu m'malo mwace.

Maweruzidwe okoma a Asa

9Ndipo caka ca makumi awiri ca Yerobiamu mfumu ya Israyeli, Asa
anayamba kukhala mfumu ya Yuda. 10Nakhala mfumu
m'Yerusalemu zaka makumi anai mphambu cimodzi, ndipo dzina la
amace linali Maaka mwana wa Abisalomu. 11Ndipo Asa anacita
zabwino pamaso pa Yehova monga Davide kholo lace. 12Nacotsa
m'dziko anyamata aja adama, nacotsanso mafano onse
anawapanga atate ace. 13Ndipo anamcotsera Maaka amace ulemu
wa mace wa mfumu, popeza iye anapanga fano lonyansitsa likhale
cifanizo; ndipo Asa analikha fano lace, nalitentha ku mtsinje wa
Kidroni. 14Koma misanje sanaicotsa, koma mtima wa Asa unali
wangwiro ndi Yehova masiku ace onse. 15Ndipo analonga
m'nyumba ya Yehova zinthu zija atate wace adazipereka; napereka
zinthu zina iye mwini zasiliva ndi zagolidi ndi zotengera.

Nkhondo ya pakati pa Asa ndi Basa

16Ndipo panali nkhondo pakati pa Asa ndi Basa mfumu ya Israyeli
masiku ao onse. 17Ndipo Basa mfumu ya Israyeli anakwera ndi
nkhondo ku Yuda, namanga ku Rama kuwaletsa anthu asaturuke
kapena kulowa kwa Asa mfumu ya Yuda. 18Tsono Asa anatenga
siliva yense ndi golidi yense anatsala pa cuma ca nyumba ya
Yehova, ndi cuma ciri m'nyumba ya mfumu, nazipereka m'manja
mwa anyamata ace; ndipo mfumu Asa anazitumiza kwa
Benihadadi mwana wa Tabrimoni, mwana wa Hezroni mfumu ya
Aramu, wakukhala ku Damasiko, nati, 19Pakhale pangano pakati pa

ine ndi inu, pakati pa atate wanga ndi atate wanu; taonani, ndatumiza kwa inu mphatso ya siliva ndi golidi, tiyeni lilekeke pangano liri pakati pa inu ndi Basa mfumu ya Israyeli, kuti andicokere. 20Ndipo Benihadadi anamvera mfumu Asa, natuma akazembe a nkhondo ace kukathira nkhondo ku midzi ya Israyeli, napasula Iyoni, ndi Dani, ndi AbeliBeti-Maaka, ndi Kineroti wonse, ndi dziko lonse la Nafitali. 21Tsono Basa atamva izi, analeka kumanga ku Rama nakhala pa Tiriza. 22Pamenepo mfumu Asa anamemeza Ayuda onse, osatsala ndi mmodzi yense; natuta miyala ya ku Rama, ndi mitengo yomwe, akamange nayo Basa; ndi mfumu Asa anamangira Geba wa ku Benjamini, ndi Mizipa. 23Ndipo macitidwe onse ena a Asa, ndi mphamvu yace yonse, ndi zonse anazicita, ndi midzi anaimanga, kodi sizilembedwa m'buku la macitidwe a mafumu a Yuda? Koma masiku a ukalamba wace anadwala mapazi ace. 24Nagona Asa ndi makolo ace, naikidwa kwa makolo ace m'mudzi wa Davide kholo lace; ndipo Yosafati mwana wace analowa ufumu m'malo mwace.

Basa akantha mbumba ya Yerobiamu nakhala mfumu ya Israyeli

25Ndipo Nadabu mwana wa Yerobiamu analowa ufumu wa Israyeli caka caciwiri ca Asa mfumu ya Yuda, nakhala mfumu ya Israyeli zaka ziwiri. 26Nacita zoipa pamaso pa Yehova, nayenda m'njira ya atate wace, ndi m'chimo lomwelo iye akacimwitsa nalo Aisrayeli. 27Ndipo Basa mwana wa Akiya, wa nyumba ya Isakara, anampangira ciwembu; ndipo Basa anamkanthira ku Gibetoni wa Afilisti, popeza Nadabu ndi Aisrayeli onse adamangira misasa Gibetoni. 28Inde Basa anamupha caka cacitatu ca Asa mfumu ya Yuda, nalowa ufumu m'malo mwace. 29Tsonokunacitika, pokhalamfumu iye, anakantha nyumba yonse ya Yerobiamu, osasiyako wamoyo ndi mmodzi yense wa Yerobiamu, kufikira adamuononga monga mwa mau a Yehova, amene analankhula pa dzanja la mtumiki wace Ahiya wa ku Silo; 30cifukwa ca macimo a Yerobiamu, amene adacimwa nao, nacimwitsa nao Aisrayeli, ndi kuutsa kwace kumene anaputa nako mkwiyo wa Yehova Mulungu wa Israyeli. 31Ndipo macitidwe ena a Nadabu, ndi zonse anazicita, kodi sizilembedwa m'buku la macitidwe a mafumu a Israyeli? 32Ndipo panali nkhondo pakati pa Asa ndi Basa mfumu ya Israyeli masiku ao onse.

33Tsono Basa mwana wa Ahiya analowa ufumu wa Israyeli caka cacitatu ca Asa mfumu ya Yuda, nakhala mfumu ku Tiriza zaka makomi awiri mphambu zinai. 34Ndipo anacimwa pamaso pa Yehova, nayenda m'njira ya Yerobiamu, ndi m'chimo lace iye anacimwitsa nalo Israyeli.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Yehu aneneratu kugwa kwa Basa

1Ndipo mau a Yehova akutsutsa Basa anadza kwa Yehu mwana wa
Hanani, nati, 2Popeza ndinakukuza iwe kucokera kupfumbi, ndi
kukuika iwe mfumu ya anthu anga Israyeli, koma iwe unayenda
m'njira ya Yerobiamu, ndi kucimwitsa anthu anga Israyeli, kuputa
mkwiyo wanga ndi macimo ao; 3taona, ndidzacotsa psiti Basa ndi
nyumba yace, ndipo ndidzafanizitsa nyumba yako ndi nyumba ya
Yerobiamu mwana wa Nebati, 4Agaru adzadya ali yense wa Basa
amene adzafera m'mudzi, ndipo amene adzafera m'thengo
zidzamudya mbalame za m'mlengalenga. 5Tsono macitidwe ena a
Basa, ndi nchito zace, ndi mphamvu zace, kodi sizilembedwa
m'buku la macitidwe a mafumu a Israyeli? 6Nagona Basa ndi
makolo ace, naikidwa ku Tiriza; ndipo Ela mwana wace analowa
ufumu m'malo mwace. 7Ndiponso mau a Yehova anadza ndi dzanja
la mneneri Yehu mwana wa Hanani, kutsutsa Basa ndi nyumba
yace, cifukwa ca zoipa zonse anazicita iye pamaso pa Yehova;
popeza anaputa mkwiyo wace ndi macitidwe a manja ace,
nafanana ndi nyumba ya Yerobiamu; ndiponso popeza anaikantha.

Ela, Zimri, ndi Omri, mafumu a Israyeli

8Ndipo caka ca makumi awiri mphambu zisanu ndi cimodzi ca Asa
mfumu ya Yuda, Ela mwana wa Basa analowa ufumu wa Israyeli ku
Tiriza, nakhala mfumu zaka ziwiri. 9Ndipo mnyamata wace Zimri,
ndiye woyang'anira dera lina la magareta ace, anampangira
ciwembu; koma iye anali m'Tiriza kumwa ndi kuledzera m'nyumba
ya Ariza, ndiye woyang'anira nyumba m'Tiriza. 10Nalowamo Zimri,
namkantha, namupha caka ca makomi awiri mphambu zisanu ndi
ziwiri ca Asa mfumu ya Yuda, nalowa ufumu m'malo
mwace. 11Ndipo kunali, atalowa ufumu wace, nakhala pa mpando
wacifumu wace, anawakantha onse a m'nyumba ya Basa,
osamsiyira mwana wamwamuna ndi mmodzi yense, kapena wa
abale ace, kapena wa mabwenzi ace. 12Motero Zimri anaononga
nyumba yonse ya Basa, monga mwa mau a Yehova, amene
ananena akumtsutsa Basa, mwa dzanja la Yehu mneneri, 13cifukwa
ca macimo onse a Basa, ndi macimo a Ela mwana wace
anacimwawo, nacimwitsa nao Aisrayeli, kuputa mkwiyo wa Yehova
Mulungu wa Israyeli ndi zacabe zao. 14Tsono macitidwe ena a Ela,
ndi nchito zace zonse, kodi sizilembedwa m'buku la macitidwe a
mafumu a Israyeli?

15Ndipo caka ca makumi awiri mphambu zisanu ndi ziwiri ca Asa
mfumu ya Yuda, Zimri anali mfumu masiku asanu ndi awiri ku
Tiriza. Ndipo anthu analikumangira misasa Gibetoni wa
Afilisti. 16Koma anthu aja omangira misasa anamva kuti Zimri
wacita ciwembu, nakanthanso mfumu; cifukwa cace tsiku lomwelo

Aisrayeli onse a kumisasa anamlonga Omri kazembe wa nkhondo akhale mfumu ya Israyeli. 17Ndipo Omri anacoka ku Gibetoni, ndi Aisrayeli onse naye, nakamangira misasa Tiriza. 18Kunali tsono, pakuona Zimri kuti nkhondo yalowa m'mudzi, anakwera pa nsanja ya nyumba ya mfumu, nadzitenthera ndi mota nyumba ya mfumu, nafa; 19cifukwa ca macimo ace anacimwawo, pakucita coipa pamaso pa Yehova; popeza anayenda m'njira ya Yerobiamu, ndi m'chimo lace anacimwa nalolo, nacimwitsa nalo Aisrayeli. 20Macitidwe ena tsono a Zimri, ndi ciwembu anacicitaco, kodi sizilembedwa m'buku la macitidwe a mafumu a Israyeli? 21Pamenepo anthu a Israyeli anagawika pakati, anthu ena anatsata Tibini mwana wa Ginati kumlonga ufumu, ena natsata Omri. 22Koma anthu akutsata Omri anapambana iwo akutsata Tibini mwana wa Ginati; nafa Tibini, Omri nakhala mfumu. 23Caka ca makumi atatu ndi cimodzi ca Asa mfumu ya Yuda, Omri anayamba kukhala mfumu ya Israyeli, nakhala zaka khumi ndi ziwiri; ku Tiriza anali mfumu zaka zisanu ndi cimodzi. 24Ndipo anagula kwa Semeri citunda ca Samaria ndi matalente awiri a siliva, namanga pacitundapo, nacha dzina lace la mudzi anaumanga Samaria, monga mwa dzina la Semeri mwini citundaco. 25Koma Omri anacimwa pamaso pa Yehova, nacita zoipa koposa onse adamtsogolerawo. 26Nayenda m'njira yonse ya Yerobiamu mwana wa Nebati, ndi chimo lace anacimwitsa nalo Aisrayeli, kuputa mkwiyo wa Yehova Mulungu wa Israyeli ndi zacabe zao. 27Ndipo macitidwe ena a Omri anawacita, ndi mphamvu yace anaionetsa, kodi sizilembedwa m'buku la macitidwe a mafumu a Israyeli? 28Nagona Omri ndi makolo ace, naikidwa m'Samaria; ndipo Ahabu mwana wace analowa ufumu m'malo mwace.

Ahabu mfumu yoipa ya Israyeli

29Ndipo caka ca makumi atatu mphambu zisanu ndi zitatu ca Asa mfumu ya Yuda Ahabu mwana wa Omri analowa ufumu wa Israyeli, nakhala Ahabu mwana wa Omri mfumu ya Israyeli m'Samaria zaka makumi awiri mphambu ziwiri. 30Ndipo Ahabu mwana wa Omri anacimwa pamaso pa Yehova koposa onse adamtsogolerawo. 31Ndipo kunali monga ngati kunamcepera kuyenda m'macimo a Yerobiamu mwana wa Nebati, iye anakwatira Yezebeli mwana wamkazi wa Etibaala mfumu ya Azidoni, natumikira Baala, namgwadira, 32Nammangira Baala guwa la nsembe m'nyumba ya Baala anaimanga m'Samaria. 33Ahabu anapanganso cifanizo; ndipo Ahabu amene anapambana mafumu onse a Israyeli adamtsogolerawo, kuputa mkwiyo wa Yehova Mulungu wa Israyeli, 34M'masiku ace Hiyeli wa ku Beteli anamanga Yeriko; pokhazika maziko ace anadzifetsera Abiramu mwana wace

woyamba, poimika zitseko zace anadzifetsera Zegubi mwana wace wotsiriza; monga mwa mau a Yehova amene ananenetsa Yoswa mwana wa Nuni.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Mneneri Eliya ku Keriti

1Ndipo Eliya wa ku Tisibe wokhala ku Gileadi ananena ndi Ahabu,
nati, Pali Yehova Mulungu wa Israyeli, amene ndimakhala pamaso
pace, ngati adzagwa mame kapena mvula zaka izi, koma ntanena
ine ndipo. 2Ndipo mau a Yehova anadza kwa iye, nati, 3Coka kuno,
nutembenukire kum'mawa, ukabisale kumtsinje Keriti uli ku
Yordano. 4Ndipo kudzakhala kuti uzikamwa mumtsinje, ndipo
ndalamulira makungubwi kukudyetsa kumeneko. 5Momwemo iye
anamuka, nacita monga mwa mau a Yehova, nakakhala kumtsinje
Keriti uli ku Yordano. 6Ndipo makungubwi anamtengera mkate ndi
nyama m'mawa, ndi mkate ndi nyama madzulo; namamwa iye
mumtsinje. 7Ndipo kunacitika, atapita masiku ena mtsinje
udaphwa, popeza munalibe mvula m'dziko.

Eliya aukitsa mwana wa wamasiye ku Zarefati

8Ndipo mau a Yehova anadza kwa iye, nati, 9Nyamuka, pita ku
Zarefati wa ku Zidoni, nukhale kumeneko; taona, ndamlamulira
mkazi wamasiye wa kumeneko akudyetse. 10Tsono iye
ananyamuka namka ku Zarefati, nafika ku cipata ca mudzi; ndipo
taona mkazi wamasiye anali kutola nkhuni; ndipo iye anamuitana,
nati, Unditengere madzi pang'ono m'cikho, ndimwe. 11Ndipo
m'mene analikumuka kukatenga iye anamuitananso, nati,
Unditengerenso kanthongo ka mkate m'dzanja lako. 12Nati iye, Pali
Yehova Mulungu wako, ndiribe mkate, koma kaufa dzanja limodzi
kali m'mbiya, ndi mafuta pang'ono m'nsupa; ndipo taona,
ndirikutola nkhuni ziwiri kuti ndikadziphikire odekha ndi mwana
wanga, tidye, tife. 13Ndipo Eliya anati kwa iye, Usacita mantha,
kacite monga umo wanenamo, koma thanga wandiocerako
kamkate, nubwere nako kwa ine; ndipo utatero udziphikire wekha
ndi mwana wako. 14Popeza atero Yehova Mulungu wa Israyeli,
Mbiya ya ufa siidzatha, ndipo nsupa ya mafuta siidzacepa, kufikira
tsiku lakugwetsa mvula Yehova pa dziko lapansi. 15Ndipo iye
anakacita monga mwa mau a Eliya, nadya iye mwini, ndi iyeyo, ndi
a m'nyumba ace, masiku ambiri. 16Mbiya ya ufa siidatha, ndi
nsupa ya mafuta siinacepa, monga mwa mau a Yehova amene
ananenetsa Eliya. 17Ndipo kunali, zitatha izi, mwana wa mkazi
mwini nyumbayo anadwala; ndipo pokula nthenda yace, analeka
kupuma. 18Ndipo mkaziyo ananena ndi Eliya, Ndiri nawe ciani
munthu iwe wa Mulungu? Kodi wadza kwa ine kundikumbutsa
chimo langa, ndi kundiphera mwana wanga? 19Ndipo ananena
naye, Ndipatse mwana wako. Namtenga m'mfukato mwace napita
naye ku cipinda cosanja cogonamo iyeyo; namgoneka pa kama wa
iye mwini. 20Napfuulira kwa Yehova, nati, Yehova Mulungu wanga,
kodi mwamgwetsera coipa mkazi wamasiye amene ndikhala naye,

kumphera mwanace? 21Nafungatira katatu pa mwanayo,
napfuulira kwa Yehova, nati, Yehova Mulungu wanga,
ndikupemphanf, ubwere moyo wace wa mwanayu m'cifuwa
mwace. 22Ndipo Yehova anamvamau a Eliya, ndipo moyo wa
mwanayo unalowanso mwa iye, nakhalanso moyo. 23Ndipo Eliya
ananyamula mwanayo, natsika naye ku cipinda cosanja, nalowa
naye m'nyumba, nampereka kwa amace; nati Eliya, Taona, mwana
wako ali moyo. 24Ndipo mkazi anati kwa Eliya, Ndizindikira tsopano
kuti ndinu munthu wa Mulungu, ndi kuti mau a Yehova ali
m'kamwa mwanuwo ngoona.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Eliya ndi Abaala ku Karimeli

1Ndipo atapita masiku ambiri, mau a Yehova anafika kwa Eliya
caka cacitatu, nati, Kadzionetse kwa Ahabu, ndipo ndidzatumiza
mvula padziko. 2Ndipo Eliya anamka kukadzionetsa kwa Ahabu.
Ndipo njala inali yaikuru m'Samaria. 3Ndipo Ahabu anaitana
Obadiya woyang'anira nyumba yace. Koma Obadiya anaopa ndithu
Yehova; 4pakuti pamene Yezebeli anapulula aneneri a Yehova,
Obadiya anatenga aneneri zana limodzi, nawabisa makumi asanu
asanu m'phanga, nawadyetsa mkate ndi madzi. 5Ndipo Ahabu
anati kwa Obadiya, Kayendere dziko lonse ku zitsime zonse
zamadzi, ndi ku mitsinje yonse, kapena tikapeza msipu ndi
kusunga moyo wa akavalo ndi nyuru, zingafe nyama zonse. 6Tsono
iwo awiri anagawana dziko kukaliyendera; Ahabu anadzera njira
yace yekha, ndi Obadiya njira yina yekha. 7Ndipo Obadiya ali
m'njira, taona, Eliya anakomana naye; iye namdziwa, namgwadira,
nati, Ndinu kodi mbuye wanga Eliya? 8Ndipo anamyankha, nati,
Ndine amene; kauze mbuye wako kuti Eliya wabwera, 9Iye nati,
Ndacimwanji kuti mupereka kapolo wanu m'dzanja la Ahabu
kundipha? 10Pali Yehova Mulungu wanu, ngati kuli mtundu umodzi
wa anthu, kapena ufumu, kumene mbuye wanga sanatumako
kukufunani, ndipo pakunena iwo, Palibe iye, analumbiritsa ufumu
umene ndi mtundu umene kuti sanakupezani. 11Ndipo tsopano
mukuti, Kauze mbuye wako kuti Eliya wabwera. 12Ndipo
kudzacitika, ine ntakusiyani, mzimu wa Yehova udzakunyamulirani
kosakudziwa ine, ndipo ine ntakauza Ahabu, ndipo akalephera
kukupezani, adzandipha. Koma ine kapolo wanu ndimaopa Yehova
kuyambira ubwana wanga. 13Kodi sanakuuzani mbuye wanga
cimene ndidacita m'kuwapha Yezebeli aneneri a Yehova, kuti ine
ndidabisa aneneri a Yehova zana limodzi makumi asanu asanu
m'phanga, ndikuwadyetsa mkate ndi madzi? 14Ndipo tsopano inu
mukuti, Kauze mbuye wako Eliya wabwera, ndipo
adzandipha. 15Koma Eliya anati, Pali Yehova wa makamu, amene
ndikhala pamaso pace, zedi, ndionekadi pamaso pace lero. 16Ndipo
Obadiya anauka kukomana ndi Ahabu, namuuza, ndipo Ahabu
ananka kukomana ndi Eliya. 17Ndipo kunacitika pamene Ahabu
anaona Eliya, Ahabu anati kwa iye Kodi ndiwe uja umbvuta
Israyeliyo? 18Nati iye, Sindimabvuta Israyeli ine ai, koma inu ndi
nyumba ya atate wanu; popeza munasiya malamulo a Yehova, ndi
kutsata Abaala. 19Ndipo tsono, tumani mundimemezere Aisrayeli
onse ku phiri la Karimeli, ndi aneneri a Baala mazana anai
mphambu makumi asanu, ndi aneneri a cifanizoco mazana anai,
akudya pa gome la Yezebeli. 20Pamenepo Ahabu anatumiza mau
kwa ana onse a Israyeli, namemeza aneneri onse ku phiri la

Karimeli. 21Ndipo Eliya anayandikira kwa anthu onse, nati, Mukayika-kayika kufikira liti? ngati Yehova ndiye Mulungu, mtsateni iye; ngati Baala, mumtsate iyeyo. Ndipo anthu nnena kumyankha mau amodzi. 22Ndipo Eliya ananena ndi anthuwo, Ine ndatsala ndekha mneneri wa Yehova, koma aneneri a Baala ndiwo anthu mazana anai mphambu makumi asanu. 23Atipatse tsono ng'ombe ziwiri; ndipo adzisankhire iwo eni ng'ombe imodzi, naiduledule, naiike pankhuni osasonkhapo moto; ndipo ine ndidzakonza ng'ombe yinayo, ndi kulika pankhuni osasonkhapo moto. 24Ndipo muitane inu dzina la mulungu wanu, ine ndidzaitana dzina la Yehova; ndipo Mulunguyo ayankhe ndi mote ndiye Mulungu. Ndipo anthu onse anabvomera, nati, Ndiwo mau abwino amene. 25Pamenepo Eliya ananena ndi aneneri a Paala, Dzisankhireni ng'ombe imodzi yanu, muyambe kuikonza, popeza mucuruka; nimuitane dzina la mulungu wanu, koma musasonkhepo moto. 26Ndipo iwo anatenga ng'ombe ija adawapatsa, naikonza, naitana dzina la Baala, kuyambira m'mawa kufikira pausana, nati, Baala, timvereni ife. Koma panalibe mau kapena wobvomereza. Ndipo anabvinabvina kuguwa adalimanga. 27Ndipo pausana Eliya anawaseka, nati, Kwezani mau, popeza ndiye mulungu; kapena alikulingirira, kapena wapambuka, kapena ali paulendo, kaya agona, adzagalamuka. 28Ndipo anakwezadi mau, nadzitema monga makhalidwe ao ndi mipeni ndi nthungo, kuti mwazi wao unali cucucu. 29Ndipo kunali, litapendeka dzuwa, ananenera kufikira nthawi ya kupereka nsembe; koma panalibe mau, kapena wobvomereza, kapena wakuwamvera. 30Pamenepo Eliya ananena ndi anthu onse, Senderani kwa ine; ndipo onse anasendera kwa iye. Iye nakonza guwa la nsembe la Yehova lidagumukalo. 31Ndipo Eliya anatenga miyala khumi ndi iwiri, monga mwa ciwerengo ca mafuko a ana a Yakobo, amene mau a Yehova adamfikira, kuti, Dzina lako ndi Israyeli. 32Ndipo ndi miyalayi anamanga guwa la nsembe m'dzina la Yehova, nazunguniza guwalo ndi mcera, ukulu wace ngati kulandira miyeso iwiri ya mbeu kuzinga guwalo. 33Ndipo anakonza nkhunizo, naduladula ng'ombe, naiika pankhuni. Nati, Dzazani madzi mbiya zinai, muwathire pa nsembe yopsereza ndi pankhuni. 34Nati, Bwerezaninso kawiri; nabwerezanso. Nati, Bwerezani katatu; nabwereza katatu. 35Ndipo madzi anayenda pozinga guwa la nsembe, nadzazanso meerawo ndi madzi. 36Ndipo kunali, nthawi ya kupereka nsembe yamadzulo, Eliya mneneri anasendera, nati, Yehova Mulungu wa Abrahamu ndi Isake ndi Israyeli, lero kudziwike kuti Inu ndinu Mulungu wa Israyeli, ndi ine mtumiki wanu, kuti mwa mau anu ndacita zonsezi. 37Ndimvereni Yehova, ndimvereni, kuti anthu awa adziwe kuti Inu Yehova ndinu

Mulungu, ndi kuti Inu mwabwezanso mitima yao. 38Pamenepo
moto wa Yehova unagwa, nutentha nsembe yopsereza, ndi nkhuni,
ndi miyala, ndi pfumbi, numwereretsa madzi anali
mumcera. 39Ndipo anthu onse anaona, nagwa nkhope zao pansi,
nati, Yehova ndiye Mulungu, Yehova ndiye Mulungu. 40Ndipo Eliya
anati kwa iwo, Gwirani aneneri a Baala, asapulumuke ndi mmodzi
yense. Nawagwira, ndipo Eliya ana pita nao ku mtsinje wa Kisoni,
nawapha pamenepo. 41Ndipo Eliya ananena ndi Ahabu,
Nyamukani, idyani, imwani; popeza kumveka mkokomo: wa mvula
yambiri. 42Ndipo Ahabu anakadya, namwa; koma Eliya anakwera
pamwamba pa Karimeli, nagwadira pansi, naika nkhope yace
pakati pa maondo ace. 43Ndipo anati kwa mnyamata wace, Kwera
kapenyerere kunyanja. Iye nakwera, napenyetsetsa, nati, Kulibe
kanthu. Nati, Bwerezanso kasanu ndi kawiri. 44Ndipo kunali
kacisanu ndi ciwiri anati, Taonani, kwaturuka kunyanja kamtambo
konga dzanja la munthu. Nati iye, Kauze Ahabu, kuti, Mangani
gareta, tsikani, mvula Ingakutsekerezeni. 45Ndipo kunali, polinda
kanthawi, thambo linada ndi mitambo ndi mphepo, nigwa mvula
yaikuru. Ndipo Ahabu anayenda m'gareta, namuka ku
Yezreeli. 46Ndipo dzanja la Yehova tinakhala pa Eliya; namanga iye
za m'cuuno mwace, nathamanga m'tsogolo mwa Ahabu ku cipata
ca Yezreeli.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Eliya athawa Yezebeli

1Ndipo Ahabu anauza Yezebeli zonse anazicita Eliya, ndi m'mene
anawaphera ndi lupanga aneneri onsewo, 2Tsono Yezebeli anatuma
mthenga kwa Eliya, wakuti, Milungu indilange nionjezepo, ngati
sindilinganiza moyo wako ndi moyo wa mmodzi wa iwowo mawa
nthawi yomwe yino. 3Ndipo iye ataona cimeneci, ananyamuka,
nathawa kupulumutsa moyo, nafika ku Beereseba wa ku Yuda,
nasiya mnyamata wace pamenepo. 4Koma iye mwini analowa
m'cipululu ulendo wa tsiku limodzi, nakakhala pansi patsinde pa
mtengo watsanya, napempha kuti afe; nati, Kwafikira, cotsani
tsopano moyo wanga, Yehova; popeza sindiri wokoma woposa
makolo anga. 5Ndipo anagona tulo patsinde pa mtengo watsanya;
ndipo taonani, wamthenga anamkhudza, nati kwa iye, Uka
nudye. 6Ndipo anaceuka, naona kumutu kunali kamkate kooca
pamakala, ndi mkhate wa madzi. Tsono anadya namwa,
nagonanso pansi, 7Ndipo mthenga wa Yehova anafikanso kaciwiri,
namkhudza, nati, Tauka, idya, popeza ulendo udzakulaka. 8Tsono
anauka, nadya namwa, nayenda ndi mphamvuya cakudya
cimeneco masiku makumi anai usana ndi usiku, nafika ku phiri la
Mulungu ku Horebu.

Eliya ku phiri la Horebu

9Nafika kuphanga, nagona kumeneko, ndipo taonani, mau a
Yehova anamfikira, nati kwa iye, Ucitanji pano, Eliya? 10Ndipo
anati, Ine ndinacitira cangu Yehova Mulungu wa makamu; popeza
ana a Israyeli anasiya cipangano canu, napasula maguwa anu a
nsembe, napha aneneri anu ndi lupanga, ndipo ndatsala ndekha,
ndipo afuna moyo wanga kuucotsa. 11Ndipo iye anati, Turuka,
nuime pa phiri tino pamaso pa Yehova. Ndipo taonani, Yehova
anapitapo, ndi mphepo yaikuru ndi yamphamvu inang'amba
mapiri, niphwanya matanthwe pamaso pa Yehova; koma Yehova
sanakhala m'mphepomo. Itapita mphepoyo kunali cibvomezi;
komanso Yehova sanali m'cibvomezico. 12Citaleka cibvomezi panali
moto; koma Yehova sanali m'motomo, Utaleka mota panali bata la
kamphepo kayaziyazi. 13Ndipo atamva Eliya, anapfunda nkhope
yace ndi copfunda cace, naturuka, naima pa khomo la phangalo.
Ndipo taonani, anamdzera mau akunena naye, Ucitanji kuno,
Eliya? 14Nati iye, Ndacitira cangu Yehova Mulungu wa makamu;
popeza ana a Israyeli ataya cipangano canu, nagumula maguwa a
nsembe anu, napha aneneri anu ndi lupanga; ndipo ndatsala
ndekha, ndipo afuna moyo wanga kuucotsa. 15Ndipo Yehova anati
kwa iye, Bwerera ulendo wako, udzere kucipululu kumka ku
Damasiko, ndipo utafikako udzoze Hazaeli akhale mfumu ya
Aramu; 16ukadzozenso Yehu mwana wa Nimsi akhale mfumu ya

Israyeli; ukadzozenso Elisa mwana wa Safati wa ku Abelimehola
akhale mneneri m'malo mwako. 17Ndipo kudzacitika Yehu
adzamupha amene adzapulumuka ku lupanga la Hazaeli; ndi Elisa
adzamupha amene adzapulumuka ku lupanga la Yehu, 18Ndiponso
ndidasiya m'Israyeli anthu zikwi zisanu ndi ziwiri osagwadira Baala
maondo ao, osampso-mpsona ndi milomo yao. 19Tsono anacokako,
napeza Elisa mwana wa Safati alikukoketsa cikhasu ng'ombe ziwiri
ziwiri magori khumi ndi awiri, iye yekha anakhala pa gori lakhumi
ndi ciwiri; ndipo Eliya anamka kunali iyeyo, naponya copfunda cace
pa iye. 20Ndipo iye anasiya ng'ombe zija, namthamangira Eliya,
nati, Ndiloleni ndithange ndakapsompsona atate wanga ndi amai
wanga; nditatero ndidzakutsatani. Nati iye, Bwerera,
ndakucitanji? 21Ndipo anabwerera panali iye uja, natengako
ng'ombe ziwiri, nazipha, naphikira nyama yace ndi zipangizo za
zocitira nazo ng'ombe, napatsa anthu adye. Atatero, ananyamuka,
natsata Eliya, namtumikira.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Nkhondo pakati pa Ahabu ndi Benihadadi

1Ndipo Benihadadi mfumu ya Aramu anamemeza khamu lace lonse la nkhondo; ndi mafumu makumi atatu mphambu awiri anali naye, pamodzi ndi akavalo ndi magareta; nakamangira Samaria misasa, naponyana nao nkhondo. 2Natumiza mithenga lrumudzi kwa Ahabu mfumu ya Israyeli, nati kwa iye, 3Atero Benihadadi, Siliva wako ndi golidi wako ndi wanga, akazi ako ndi ana ako omwe okometsetsawo ndi anga. 4Ndipo mfumu ya Israyeli anayankha, nati, Monga mwanena, mbuye wanga mfumu, ndine wanu ndi zonse ndiri nazo. 5Tsono mithenga ija inabwerera, niti, Atero Benihadadi, kuti, Ndinatumadi kwa iwe, ndi kuti, Uzindipatsa siliva wako, ndi golidi wako, ndi akazi ako, ndi ana ako; 6koma mawa dzuwa lino ndidzatuma anyamata anga kwa iwe, nadzafunafuna m'nyumba mwako, ndi m'nyumba za anyamata ako; ndipo kudzakhala kuti cifuniro conse ca maso ako adzacigwira ndi manja ao, nadzacicotsa. 7Pamenepo mfumu ya Israyeli anaitana akulu onse a dziko, nati, Tazindikirani inu, penyani kuti-munthu uyu akhumba coipa; popeza anatuma kwa ine kulanda akazi anga, ndi ana anga, ndi siliva, ndi golidi wanga; ndipo sindinamkaniza. 8Ndipo akulu onse ndi anthu onse anati kwa iye, Musamvere, musabvomereze. 9Ndipo anati kwa mithenga ya Benihadadi, Kauzeni mbuye wanga mfumu, Zonse munayamba kundituma mtumiki wanu kuzifunsa ndidzacita, koma ici sindingacicite. Nicoka mithengayo, nimbwezera mau. 10Ndipo Benihadadi anatuma kwa iye, nati, Milungu indilange, nionjezepo, ngati pfumbi la Samaria lidzafikira kudzaza manja a anthu onse akutsata mapazi anga. 11Ndipo mfumu ya Israyeli anayankha, nati, Kamuuzeni, Wakumanga zida asadzikuze ngati wakubvulayo. 12Ndipo kunacitika, atamva Benihadadi mau awa, analikumwa nao mafumu m'misasa, ananena ndi anyamata ace, Nikani. Nandandalika pamudzipo. 13Ndipo taonani, mneneri anadza kwa Ahabu mfumu ya Israyeli, nati, Atero Yehova, Kodi waona unyinji uwu waukuru wonse? Taonani, ndidzaupereka m'dzanja mwako lero, kuti udziwe kuti ndine Yehova. 14Nati Ahabu, Mwa yam? Nati, Atero Yehova, Mwa anyamata a akalonga a madera. Natinso, Adzayamba kuponya nkhondo ndani? Nati, Iwe. 15Pamenepo anawerenga anyamata a akalonga a madera, nawapeza mazana awiri mphambu makumi atatu kudza awiri. Pamenepo anawerenganso anthu onse, ndiwo ana a Israyeli onse zikwi zisanu ndi ziwiri. 16Ndipo amenewo anaturuka usana. Koma Benihadadi analinkumwa naledzera m'misasamo, iye ndi mafumu aja makumi atatu mphambu awiri aja akumthandiza. 17Ndipo anyamata a akalonga a madera anayamba kuturuka, koma

Benihadadi anatuma anthu, iwo nambwezera mau, kuti, M'Samaria mwaturuka anthu. 18Nati iye, Cinkana aturukira mumtendere, agwireni amoyo; cinkana aturukira m'nkhondo, agwireni amoyo. 19Tsono anaturuka m'mudzi anyamata a akalonga a madera aja, ndi khamu la nkhondo linawatsata. 20Ndipo ali yense anapha munthu wace; ndipo Aaramu anathawa, Aisrayeli nawapitikitsa; ndipo Benihadadi mfumu ya Aramu anathawira pa kavalo pamodzi ndi apakavalo. 21Tsono mfumu ya Israyeli inaturuka, nikantha apakavalo ndi apamagareta, nawapha Aaramuwo maphedwe akuru. 22Ndipo mneneri uja anayandikira kwa mfumu ya Israyeli, nati kwa iye, Kadzilimbitseni, mudziwe mucenjere ndi cimene mucicita; popeza caka cikudzaci mfumu ya Aramu idzabweranso kulimbana nanu.
23Ndipo anyamata a mfumu ya Aramu anati kwa iye, Milungu yao nja kumapiri, ndimo m'mene atilakira; koma tikaponyana nao kucidikha, zedi tidzaposa mphamvu. 24Tsono citani ici, cotsani mafumu aja yense ku malo ace, muike m'malo mwao akazembe. 25Ndipo mudziwerengere khamu la nkhondo longa khamu lija lidaonongekalo, ndi akavalo onga akavalo aja, ndi magareta monga omwe aja; ndipo tikaponyane nao pacidikha tidzawapambana ndithu. Namvera iye mau ao, natero kumene. 26Tsono kunacitika, pakufikanso caka Benihadadi anamemeza Aaramu nakwera ku Meld kukaponyana ndi Aisrayeli. 27Ndipo Aisrayeli anamemezananso, anali naye kamba, nakakomana nao; ndipo Aisrayeli anamanga misasa yao pandunji pao, ngati timagulu tiwiri ta ana a mbuzi; koma Aaramu anadzaza dziko. 28Ndipo munthu uja wa Mulungu anafikako, nalankhula ndi mfumu ya Israyeli, nati, Atero: Yehova, Popeza Aaramu amati, Yehova ndiye Mulungu wa kumapiri, osati Mulungu wa kuzigwa, mwa ici ndidzapereka unyinji uwu waukuru m'dzanja mwako, kuti mudziwe kuti Ine ndine Yehova. 29Ndipo awa anakhala m'misasa pandunji pa ajawo masiku asanu ndi awiri. Tsono kunali, tsiku lacisanu ndi ciwiri anayambana nkhondo; ndipo ana a Israyeli anaphako Aaramu tsiku limodzi anthu oyenda pansi zikwi zana limodzi. 30Ndipo otsalawo anathawira ku Afeki kumudzi, ndipo linga linawagwera anthu zikwi makumi awiri mphambu asanu ndi awiri amene adatsalawo. Ndipo Benihadadi anathawa, nalowa m'mudzi, m'cipinda ca m'katimo. 31Pamenepo anyamata ace anati kwa iye, Taonani, tidamva ife kuti mafumu a nyumba ya Israyeli ndi mafumu acifundo; tiyeni tibvale ciguduli m'cuuno mwathu, ndi zingwe pamitu pathu, titurukire kwa mfumu ya Israyeli, kapena adzakusungirani moyo. 32Motero anabvala ciguduli m'cuuno mwao, ndi zingwe pamitu pao, nafika kwa mfumu ya Israyeli, nati, Kapolo wanu Benihadadi ati, Ndiloleni ndikhale ndi moyo. Nati iye, Akali

moyo kodi? Ndiye mbale wanga. 33Tsono anthuwo
anamyang'anitsa, nafulumira kugwira mauwo ngati anaterodi; nati,
Mbale wanu Benihadadi ali moyo, Nati, Kamtengeni, Pamenepo
Benihadadi anaturuka, nadza kwa iye, ndipo iye anamkweza
m'gareta mwaceo 34Ndipo Benihadadi anati kwa iye, Ndidzabweza
midzi ija atate wanga analanda kwa atate wanu; ndipo
mudzikonzere mabwalo a malonda m'Damasiko, monga umo atate
wanga anadzikonzera m'Samaria. Ndi ine, ati Ahabu, ndikulola
umuke ndi pangano ili. Tsono anapangana naye, namlola amuke.
35Ndipo wina wa ana a aneneri ananena ndi mnzace mwa mau a
Yehova, Undikanthe ine, Koma munthuyo anakana
kumkantha. 36Ndipo ananena naye, Popeza sunamvera mau a
Yehova, taona, utalekana nane mkango udzakupha, Ndipo m'mene
atalekana naye, mkango unampeza, numupha. 37Ndipo amene uja
anakomana ndi munthu wina, nati, Undikanthe. Namkantha
munthuyu, namtema pomkantha. 38Pamenepo mneneriyo
anamuka, nadikira mfumu pamseu, nadzizimbaitsa ndi mpango
pamaso pace. 39Ndipo popitapa mfumu, anapfuula kwa mfumu,
nati, Kapolo wanu analowa pakati pa nkhondo, ndipo taonani,
munthu anapambuka nabwera ndi munthu kwa ine, nati, Tasunga
munthu uyu; akasowa ndi cifukwa ciri conse moyo wako udzakhala
m'malo mwa moyo wace, kapena udzalipa talenti la siliva. 40Tsono
pocita kapolo wanu apo ndi apo ndapeza palibe. Ndipo mfumu ya
Israyeli inati kwa iye, Mlandu wako ukutsutsa momwemo,
wadziweruza wekha. 41Ndipo iye anafulumira kucotsa mpango
kumaso kwace, ndi mfumu ya Israyeli inaona kuti anali mmodzi wa
aneneri. 42Niti kwa iye, Atero Yehova, Popeza wataya m'dzanja lako
munthu uja ndinati ndimuononge konse, moyo wako udzakhala
m'malo mwamoyo wace, ndi anthu ako m'malo mwa anthu
ace. 43Pamenepo mfumu ya Israyeli inamka kwao wamsunamo ndi
wokwiya, nafika ku Samaria.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Yezebeli aphetsa Naboti

1Ndipo zitatha izi, kunaoneka zotere: Naboti wa ku Yezreeli anali
ndi munda wamphesa, unali m'Yezreelimo, m'mbali mwa nyumba
ya Ahabu mfumu ya ku Samaria. 2Ndipo Ahabu analankhula ndi
Naboti, nati, diloleni Ndipatse munda wako wamphesa ukhale
munda wanga wa ndiwo, popeza uli pafupi ndi nyumba yanga;
ndipo m'malo mwace ndidzakupatsa munda wamphesa wokoma
woposa uwu; kapena kukakukomera ndidzakupatsa ndalama za pa
mtengo wace, 3Ndipo Naboti anati kwa Ahabu, Pali Yehova, ndi
pang'ono ponse ai, kuti ndikupatseni colowa ca makolo
anga, 4Ndipo Ahabu analowa m'nyumba mwace wamsunamo ndi
wokwiya, cifukwa ca mau amene Naboti wa ku Yezreeli
adalankhula naye; popeza adati, Sindikupatsani colowa ca makolo
anga. M'mwemo anagona pa kama wace, nayang'ana kumbali,
nakana kudya mkate. 5Koma Yezebeli mkazi wace anadza kwa iye,
nati kwa iye, Mucitiranji msunamo, kuti mukana kudya
mkate? 6Nati kwa iye, Popeza ndinalankhula kwa Naboti wa ku
Yezreeli, ndinati kwa iye, Undigulitse munda wako ndi ndalama;
kapena ukafuna, ndikupatsa munda wina m'malo mwace; kama
anandiyankha, Sindikupatsani munda wanga wamphesa. 7Ndipo
Yezebeli mkazi wace anati kwa iye, Kodi mulamulira Aisrayeli
tsopano ndinu? Taukani, idyani mkate, ukondwere mtima wanu;
munda wa Naboti wa ku Yezreeli ndidzakupatsani
ndine. 8M'mwemo analemba akalata m'dzina la Ahabu
nakhomerapo cizindikilo cace, natumiza akalatawo kwa akulu ndi
omveka anali m'mudzi mwace, nakhala naye Naboti. 9Ndipo
analemba m'akalata, nati, Lalikirani kuti asale kudya, muike Naboti
pooneka ndi anthu; 10ndipo muike anthu awiri, anthu oipa, pamaso
pace, kuti amcitire umboni, ndi kuti, Watemberera Mulungu ndi
mfumu; nimumturutse ndi kumponya miyala kumupha. 11Ndipo
anthu aja a mudzi wace, ndiwo akulu ndi omveka adakhala
m'mudzi mwace, anacita monga Yezebeli anawatumizira, monga
munalembedwa m'akalata amene iye anawatumizira. 12Analalikira
kuti asale kudya, naike Naboti pooneka ndi anthu. 13Ndipo anthu
aja awiri oipawo analowa, nakhala pamaso pace, ndipo anthu
oipawo anamcitira umboni wonama Nabotiyo, pamaso pa anthu
onse, nati, Naboti anatemberera Mulungu ndi mfumu. Pamenepo
anamturutsa m'mudzi, namponya miyala, namupha. 14Pomwepo
anatuma mau kwa Yezebeli, nati, Naboti waponyedwa miyala,
nafa. 15Ndipo kunali, atamva Yezebeli kuti anamponya Naboti
miyala nafa, Yezebeli anati kwa Ahabu, Taukani, landirani munda
wamphesa wa Naboti Myezreeli uja anakana kukugulitsani ndi
ndarama, popeza, Naboti sali ndi moyo, koma wafa. 16Ndipo kunali,

atamva Ahabu kuti Naboti wafa, Ahabu anauka kukatsikira ku munda wamphesa wa Naboti, kuulandira.

Eliya auza Ahabu za kuonongeka kwa mbumba yace

17Ndipo mau a Yehova anadza kwa Eliya waku Tisibe,
nati, 18Nyamuka, tsikira kukakomana ndi Ahabu mfumu ya Israyeli,
akhala m'Samariya; taona, ali ku munda wamphesa wa Naboti
kumene anatsikira kukaulandira. 19Ndipo uzilankhula naye, ndi
kuti, Atero Yehova, Kodi wapha, mulandanso? Nulankhulenso naye,
kuti, Atero Yehova, Paja agaru ananyambita mwazi wa Naboti,
pompaja agaru adzanyambita mwazi wako, inde wako. 20Ndipo
Ahabu anati kwa Eliya, Wandipeza kodi, mdani wangawe?
Nayankha, Ndakupeza; pokhala wadzigulitsa kucita coipaco
pamaso pa Yehova. 21Taona, ndidzakufikitsira coipa, ndi kucotsa
mbumba yako psiti; ndipo ndidzalikhira Ahabu mwana
wamwamuna yense, ndi yense womangika ndi womasuka
m'Israyeli; 22ndipo ndidzalinganiza nyumba yako ndi nyumba ya
Yerobiamu mwana wa Nebati, ndi ya Basa mwana wa Ahiya;
cifukwa ca kuputa kumene unaputa nako mkwiyo wanga, ndi
kucimwitsa Israyeli. 23Ndipo za Yezebeli yemwe Yehova ananena,
nati, Agaru adzadya Yezebeli ku linga la Yezreeli. 24Mwana ali
yense wa Ahabu amene adzafera m'mudzi, agaru adzamudya;
ndipo iye amene adzafera kuthengo, mbalame za m'mlengalenga
zidzamudya, 25Koma panalibe wina ngati Ahabu wakudzigulitsa
kucita coipa pamaso pa Yehova, amene Yezebeli mkazi wace
anamfulumiza. 26Ndipo anacita moipitsitsa kutsata mafano, monga
mwa zonse amazicita Aamori, amene Yehova adawapitikitsa
pamaso pa ana a Israyeli. 27Ndipo kunali, pakumva Ahabu mau
amenewa, anang'amba zobvala zace, nabvala ciguduli pathupi
pace, nasala kudya, nagona paciguduli, nayenda
nyang'anyang'a. 28Pamenepo mau a Yehova anadza kwa Eliya wa
ku Tisibe, nati, 29Waona umo wadzicepetsera Ahabu pamaso
panga? Popeza adzicepetsa pamaso panga, sindidzafikitsa coipa
cimeneci akali moyo iye; koma m'masiku a mwana wace
ndidzacifikitsa pa nyumba yace.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Ahabu apangana ndi Yehosafati

1Ndipo Aaramu ndi Aisrayeli anakhala cete zaka zitatu, osathirana
nkhondo. 2Koma kunacitika caka cacitatu, kuti Yehosafati mfumu
ya Yuda anatsikira kwa mfumu ya Israyeli. 3Ndipo mfumu ya
Israyeli ananena ndi anyamata ace, nati, Kodi simudziwa kuti
Ramoti Gileadi ngwathu, ndipo tangokhala cete, osaulanditsa
m'dzanja la mfumu ya Aramu. 4Tsono anati kwa Yehosafati, Kodi
udzapita nane kunkhondo ku Ramoti Gileadi? Ndipo Yehosafati
anati kwa mfumu ya Israyeli, M'mene ukhalira iwe ndi momwe
ndikhalira ndine; anthu anga monga anthu ako, akavalo anga
monga akavale ako. 5Ndipo Yehosafati ananena ndi mfumu ya
Israyeli, Fuusira ku mau a Yehova lero. 6Pamenepo mfumu ya
Israyeli inasonkhanitsa aneneri ngati anthu mazana anai, nanena
nao, Kodi ndizimuka kukathira nkhondo pa Ramoti Gileadi, kapena
ndileke? Nati iwo, Kweraniko; popeza Ambuye adzaupereka
m'dzanja la mfumu. 7Koma Yehosafati anati, Kodi pano palibe
mneneri wina wa Yehova, kuti tifunsire kwa iye? 8Ndipo mfumu ya
Israyeli inati kwa Yehosafati, Alipo munthu wina kuti tifunsire kwa
Yehova mwa iye; koma ndimuda, popeza samanenera za ine
zabwino, koma zoipa; ndiye Mikaya mwana wace wa Yimla. Nati
Yehosafati, Isamatero mfumu. 9Tsono mfumu ya Israyeli anaitana
mdindo, nati, Kamtenge msanga Mikaya mwana wa Yimla. 10Ndipo
mfumu ya Israyeli ndi Yehosafati mfumu ya Yuda anakhala onse
awiri, yense pa mpando wacifumu wace, obvala zobvala zao
zacifumu pabwalo pa khomo la cipata ca Samaria; ndipo aneneri
onse ananenera pamaso pao. 11Ndipo Zedekiya mwana wa Kenana
anadzisulira nyanga zacitsulo, nati, Atero Yehova, Ndi izi
mudzagunda nazo Aaramu mpaka atatha psiti, 12Ndipo aneneri
onse ananena momwemo, nati, Kwerani ku Ramoti Gileadi, ndipo
mudzacita mwai; popeza Yehova adzaupereka m'dzanja la mfumu.

Mikaya anenera motsutsa Ahabu

13Tsono mthenga uja udakaitana Mikaya unanena naye, nati,
Taona, mau a aneneri abvomerezana zokoma kwa mfumu ndi
m'kamwa m'modzi; mau ako tsono afanane ndi mau a wina wa
iwowo, nunene zabwino. 14Koma Mikaya anati, Pali Yehova, zimene
Yehova adzanena nane ndidzanena ine. 15Ndipo atafika kwa
mfumu, mfumu inati kwa iye, Mikaya, kodi tizimuka ku Ramoti
Gileadi kukathira nkhondo, kapena tileke? Nati iye, Kwerani, ndipo
mudzacita mwai, popeza Yehova adzaupereka m'dzanja la
mfumu. 16Ndipo mfumu inati, Ndikulumbiritse kangati kuti undiuze
zoona zokha zokha m'dzina la Yehova? 17Nati iye, Ndinaona
Aisrayeli onse obalalika pamapiri ngati nkhosa zopanda mbusa;
ndipo Yehova anati, Izi ziribe mwini, yense abwerere ndi mtendere

ku nyumba yace. 18Pamenepo mfumu ya Israyeli inanena ndi Yehosafati, Kodi sindinakuuza kuti uyu sadzanenera za ine zabwino, koma zoipa? 19Ndipo anati, Cifukwa cace tamverani mau a Yehova, Ndinaona Yehova alikukhala pa mpando wace wacifumu, ndi khamu lonse la Kumwamba liri ciriri m'mbali mwace, ku dzanja lamanja ndi lamanzere, 20Nati Yehova, Adzanyenga Ahabu ndani, kuti akwere nagwe ku Ramoti Gileadi? Ndipo anati wina mwakuti, wina mwakuti. 21Pamenepo mzimu wina unaturuka, nuima pamaso pa Yehova, nuti, Ndidzamnyenga ndine. Nati Yehova kwa iye, Motani? 22Nati, Ndidzaturuka, ndidzakhala mzimu wonama m'kamwa mwa aneneri ace onse. Nati, Udzamnyengadi, nudzakhozanso; turuka, ukatero kumene. 23Ndipo tsopano taonani, Yehova waika mzimu wonama m'kamwa mwa aneneri anu onse awa, ndipo Yehova ananena coipa ca inu. 24Pamenepo Zedekiya mwana wa Kenana anasendera, napanda Mikaya patsaya, nati, Mzimu wa Yehova wandicokera bwanji, kulankhula ndi iwe? 25Mikaya nati, Taona, udzapenya tsiku lolowa iwe m'cipinda ca pakati kubisala. 26Pamenepo inati mfumu ya Israyeli, Tengani Mikaya, mumbweze kwa Amoni kalonga wa mudzi, ndi kwa Yoasi mwana wa mfumu; 27ndipo muziti, Itero mfumu, Khazikani uyu m'kaidi, mumdyetse cakudya ca nsautso, ndi madzi a nsautso, mpaka ndikabwera ndi mtendere. 28Ndipo Mikaya anati, Mukabwera ndithu ndi mtendere Yehova sanalankhula mwa ine. Nati, Mvetsani, anthu inu nonse.

Ahabu aphedwa mu nkhondo ya pa Aramu

29Tsono mfumu ya Israyeli ndi Yehosafati mfumu ya Yuda anakwera ku Ramoti Gileadi. 30Ndipo mfumu ya Israyeli inanena ndi Yehosafati, Ine ndidzadzizimbaitsa, ndi kulawa kunkhondo, koma bvala iwe zobvala zako zacifumu. Ndipo mfumu ya Israyeli inadzizimbaitsa, nilowa kunkhondo. 31Tsono mfumu ya Aramu idalamulira akapitao makumi atatu mphambu ziwiri za magareta ace, niti, Musaponyana ndi anthu ang'ono kapena akuru, koma ndi mfumu ya Israyeli yokha. 32Ndipo kunali, akapitao a magareta ataona Yehosafati, anati, Zedi uyu ndiye mfumu ya Israyeli imene, napotolokera kukaponyana naye; koma Yehosafati anapfuula. 33Ndipo pamene akapitao a magareta anaona kuti sindiye mfumu ya Israyeli, anabwerera osampitikitsa. 34Ndipo munthu anakoka uta wace ciponyeponye, nalasa mfumu ya Israyeli pakati pa maluma a maraya acitsulo; tsono ananena ndi mnyamata wa gareta wace, Tembenuza dzanja lako, nundicotse kunkhondo, popeza ndalasidwa. 35Ndipo nkhondo inakula tsiku lomwelo, ndipo mfumu inagwirizidwa m'gareta mwace kupenyana ndi Aaramu, natsirizika madzulo; ndipo mwazi unaturuka m'bala pa phaka la gareta. 36Ndipo mfuu unafikira khamu lonse la nkhondo

polowa dzuwa, ndi kuti, Yense kumudzi kwao, ndi yense ku dziko la kwao. 37Ndipo inafa mfumu, naifikitsa ku Samaria, naika mfumu m'Samaria. 38Ndipo potsuka garetayo pa thawale la ku Samaria agaru ananyambita mwazi wace, pala pamasamba akazi adama, monga mwa mau a Yehova amene ananenawo. 39Tsono macitidwe ena a Ahabu, ndi zonse adazicita, ndi nyumba ya minyanga adaimanga, ndi midzi yonse adaimanga, kodi sizilembedwa m'buku la macitidwe a mafumu a Israyeli? 40Ndipo Ahabu anagona ndi makolo ace; ndi Ahaziya mwana wace anakhala mfumu m'malo mwace.

Yehosafati mfumu ya Yuda

41Koma Yehosafati mwana wa Asa anayamba kukhala mfumu ya Yuda caka cacinai ca Ahabu mfumu ya Israyeli. 42Yehosafati anali wa zaka makumi atatu mphambu zisanu, pamene analowa ufumu, nakhala nifumu zaka makumi awiri mphambu zisanu m'Yerusalemu. Ndi dzina la amace linali Azuba mwana wa Sili. 43Ndipo anayenda m'njira yonse ya atate wace Asa, osapambukamo; nacita coyenera pamaso pa Yehova, koma misanje sanaicotsa; anthu anapherabe nsembe, nafukiza zonunkhira pamsanje. 44Ndipo Yehosafati anacitana mtendere ndi mfumu ya Israyeli. 45Tsono maciddwe ena a Yehosafati, ndi mphamvu anaionetsayo, ndi umo anathira nkhondo, kodi sizilembedwa m'buku la macitidwe a mafumu a Yuda? 46Ndipo anacotsa m'dziko anyamata onyansa aja adatsalira masiku a atate wace Asa. 47Ndipo m'Edomu munalibe mfumu, koma kazembe wa mfumu. 48Yehosafati anamanga zombo za ku Tarsisi kukatenga golidi ku Ofiri; koma sizinamuka, popeza zinaphwanyika pa Ezioni Geberi. 49Pamenepo Ahaziyamwana wa Ahabu ananena ndi Yehosafati, Anyamata anga amuke pamodzi ndi anyamata anu m'zombo. Koma Yehosafati anakana. 50Ndipo Yehosafati anagona ndi makolo ace, naikidwa ndi makolo ace m'mudzi wa Davide kholo lace; ndipo Yoramu mwana wace anakhala mfumu m'malo mwace.

Ahaziya mfumu ya Israyeli

51Ahaziya mwana wa Ahabu anayamba kukhala mfumu ya Israyeli pa Samaria m'caka cakhumi mphambu zisanu ndi ziwiri ca Yehosafati mfumu ya Yuda; nakhala mfumu ya Israyeli zaka ziwiri. 52Nacita coipa pamaso pa Yehova, nayenda m'njira ya atate wace, ndi ya amace, ndi ya Yerobiamu mwana wa Nebati, amene adacimwitsa Israyeli. 53Natumikira Baala, namweramira, naputa mkwiyo wa Yehova Mulungu wa Israyeli, monga umo anacitira atate wace.

©The Bible Society of Malawi, 1992

2 Kings

2 Mafumu 1

Eliya ndi nthenda ya Ahaziya

1NDIPO atamwalira Ahabu, Moabu anapandukana ndi
Israyeli. 2Ndipo Ahaziya anagwa kubzola ku made wa cipinda cace
cosanja cinali ku Samariya, nadwala, natuma mithenga, nanena
nayo, Mufunsire kwa Baala Zebubu mulungu wa ku Ekroni ngati
ndidzacira nthenda iyi. 3Koma mthenga wa Yehova anati kwa Eliya
wa ku Tisibe, Nyamuka, kwera kukomana ndi mithenga ya mfumu
ya Samariya, nunene nayo, Kodi ndi popeza palibe Mulungu mwa
Israyeli, kuti mukafunsira kwa Baala Zebubu mulungu wa ku
Ekroni? 4Cifukwa cace atero Yehova, Sudzatsika pakama pamene
wakwerapo, koma udzafa ndithu. Nacoka Eliya. 5Ndipo mithenga
inabwerera kwa iye, nanena nayo, Mwabwerera cifukwa
ninji? 6Ndipo inanena naye, Munthu anakwera kukomana nafe, nati
kwa ife, Kabwerereni kwa mfumu imene inakutumani inu,
nimunene nayo, Atero Yehova, Kodi ndi popeza palibe Mulungu
mwa Israyeli, kuti ulikutuma kukafunsira kwa Baala Zebubu
mulungu wa ku Ekroni? Cifukwa cace sudzatsika pakama pamene
wakwerapo, koma udzafa ndithu. 7Ndipo iye ananena nayo, Nanga
maonekedwe ace a munthu anakwerayo kukomana nanu, nanena
nanu mau awa, ndi otani? 8Ninena naye, Ndiye munthu wobvala
zaubweya, namangira m'cuuno mwace ndi lamba lacikopa. Nati
iye, Ndiye Eliya wa ku Tisibe. 9Pamenepo mfumu inatuma kwa iye
asilikari makumi asanu ndi mtsogoleri wao. Iye nakwera kumka
kwa Eliya; ndipo taonani, analikukhala pamwamba pa phiri. Ndipo
analankhula naye, Munthu wa Mulungu iwe, mfumu ikuti,
Tsika. 10Nayankha Eliya, nanena ndi mtsogoleriyo, Ndikakhala ine
munthu wa Mulungu, utsike mota wakumwamba, nunyeketse iwe
ndi makumi asanu ako. Pamenepo unatsika mota kumwamba,
nunyeketsa iye ndi makumi asanu ace. 11Ndipo anabwereza
kutuma kwa iye mtsogoleri wina ndi makumi asanu ace. Ndipo iye
anayankha nanena naye, Munthu wa Mulungu iwe, itero mfumu,
Tsika msanga. 12Nayankha Eliya, nanena nao, Ndikakhala ine
munthu wa Mulungu, utsike mota wakumwamba, nunyeketse iwe
ndi makumi asanu ako. Pamenepo mota wa Mulungu unatsika
kumwamba nunyeketsa iye ndi makumi asanu ace. 13Ndipo
anabwerezaaso kutuma mtsogolen wacitatu ndi makumi asanu
ace. Nakwera mtsogoleri wacitatuyo, nadzagwada ndi maondo ace
pamaso pa Eliya, nampembedza, nanena naye, Munthu wa
Mulungu inu, ndikupemphani, moyo wanga ndi moyo wa anyamata
anu makumi asanu awa akhale a mtengo wace pamaso
panu. 14Taonani, watsika mota wakumwamba, nunyeketsa

atsogoleri awiri oyamba aja pamodzi ndi makumi asanu ao; koma tsopano moyo wanga ukhale wa mtengo wace pamaso panu. 15Pamenepo mthenga wa Yehova anati kwa Eliya, Tsika naye, usamuopa. Nanyamuka iye, natsikira naye kwa mfumu. 16Ndipo ananena nayo, Atero Yehova, Popeza watuma mithenga kukafunsira kwa Baala Zebubu mulungu wa ku Ekroni, kodi ndi popeza palibe Mulungu mwa Israyeli kufunsira mau ace? Cifukwa cace sudzatsika pakama pamene wakwerapo, koma udzafa ndithu. 17Motero anafa monga mwa mau a Yehova adanena Eliyawo. Ndipo Yehoramu analowa ufumu m'malo mwace caka caciwiri ca Yehoramu mwana wa Yehosafati mfumu ya Yuda, pakuti analibe mwana wamwamuna. 18Macitidwe ace ena tsono adawacita Ahaziya, kodi salembedwa m'buku la macitidwe a mafumu a Israyeli?

©The Bible Society of Malawi, 1992

Eliya atengedwa kunka Kumwamba

1Ndipo kunali, pamene Yehova adati akweze Eliya kumwamba ndi
kabvumvulu, Eliya anacokera ku Giligala pamodzi ndi Elisa. 2Ndipo
Eliya anati kwa Elisa, Ukhale pompano pakuti Yehova wandituma
ndimke ku Beteli. Nati Elisa, Pali Mulungu, pali inu, sindikusiyani.
Motero anatsikira iwo ku Beteli. 3Ndipo ana a aneneri okhala ku
Beteli anaturukira Elisa, nanena naye, Kodi udziwa kuti Yehova
akucotsera lero mbuye wako, mtsogoleri wako? Nati, lode
ndidziwa, khalani muli cete. 4Ndipo Eliya anati kwa iye, Elisa,
ukhale pompano, pakuti Yehova wandituma ku Yeriko. Nati iye, Pali
Yehova, pali inu, sindikusiyani. Motero anadza ku
Yeriko. 5Pamenepo ana a aneneri okhala ku Yeriko anayandikira
kwa Elisa, nanena naye, Kodi udziwa kuti Yehova akucotsera lero
mbuye wako, mtsogoleri wako? Nati iye, Inde ndidziwa, khalani
muli cete. 6Ndipo Eliya ananena naye, Ukhale pompano, pakuti
Yehova wandituma ku Yordano, Nati iye, Pali Mulungu, pali inu,
sindikusiyani. Napitirira iwo awiri. 7Ndipo anthu makumi asanu a
ana a aneneri anapita, naima patali pandunji pao, iwo awiri naima
ku Yordano. 8Ndipo Eliya anagwira copfunda cace, nacipindapinda
napanda madzi, nagawikana kwina ndi kwina; ndipo anaoloka iwo
onse awiri pansi pouma. 9Ndipo kunali ataoloka, Eliya anati kwa
Elisa, Tapempha cimene ndikucitire ndisanacotsedwe kwa iwe.
Ndipo Elisa anati, Mundipatse magawo awiri a mzimu wanu akhale
pa ine. 10Nati iye, Wapempha cinthu capatali, koma ukandipenya
pamene ndicotsedwa kwa iwe, kudzatero nawe; koma ukapanda
kundipenyapo, sikudzatero at. 11Ndipo kunacidka, akali ciyendere
ndi kukambirana, taonani, anaoneka gareta wamoto ndi akavalo
amoto, nawalekanitsa awiriwa; Eliya nakwera kumwamba ndi
kabvumvulu. 12Ndipo Elisa anapenya, napfuula, Atate wanga, atate
wanga, gareta wa Israyeli ndi apakavalo ace! Koma analibe
kumpenyanso; nagwira zobvala zace zace, nazing'amba pakati.

Elisa mneneri, zozizwitsa zace

13Pamenepo anatola copfunda cace ca Eliya cidamtayikiraco,
nabwerera, naima m'mphepete mwa Yordano. 14Ndipo anatenga
copfunda ca Eliya cidamtayikiraco, napanda madziwo, nati, Ali kuti
Yehova Mulungu wa Eliya? Ndipo atapanda madziwo anagawikana
kwina ndi kwina, naoloka Elisa. 15Ndipo pamene anampenya ana a
aneneri okhala ku Yeriko pandunji pace, anati, Mzimu wa Eliya
watera pa Elisa. Ndipo anadza kukomana naye, nadziweramitsa
pansi kumaso kwace. 16Ndipo ananena naye, Taonani, tsono
anyamata anufe tiri nao amuna makumi asanu amphamvu, amuke
kukafuna mbuye wanu; kapena wamkweza mzimu wa Yehova ndi
kumponya pa phiri lina, kapena m'cigwa dna. Koma anati,

Musatumiza. 17Koma anamuumiriza kufikira anacita manyazi;
pamenepo anati, Tumizani. Motero anatumiza amuna makumi
asanu, namfunafuna iwo masiku atatu, osampeza. 18Nabwerera
kwa iye ali cikhalire ku Yeriko, ndipo anati kwa iwo, Kodi
sindinanena nanu, Musamuka?
19Ndipo amuna a kumudzi anati kwa Elisa, Taonani, pamudzi pano
mpabwino, monga umo aonera mbuye wanga; koma madzi ndi
oipa, ndi nthaka siibalitsa. 20Pamenepo anati, Nditengereni
cotengera catsopano, muikemo mcere. Ndipo anabwera naco kwa
iye. 21Ndipo anaturuka kumka ku magwero a madzi, nathiramo
mcere, nati, Atero Yehova, Ndaciritsa madzi awa,
sikudzafumirakonso imfa, kapena kusabalitsa. 22Cotero madzi
anaciritsidwa mpaka lero lino, monga mwa mau a Elisa
ananenawo.
23Ndipo anacokako kukwera ku Beteli, ndipo iye ali cikwerere
m'njiramo, munaturuka anyamata ang'ono m'mudzimo, namseka,
nati kwa iye, Takwera wadazi, takwera wadazi! 24Ndipo anaceuka,
nawaona, nawatemberera m'dzina la Yehova. Ndipo kuthengo
kunaturuka zimbalangondo ziwiri zazikazi, ndi kupwetedza mwa
iwo ana makumi anai mphambu awiri. 25Ndipo anacokako kumka
ku phiri la Karimeh; nabwera kumeneko nafika ku Samariya.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Cipulumutso codabwitsa ca nkhondo za Yuda, Israyeli, ndi Edomu

1Ndipo Yehoramu mwana wa Ahabu analowa ufumu wa Israyeli
m'Samariya m'caka cakhumi mphambu zisanu ndi zitatu ca
Yehosafati mfumu ya Yuda, nakhala mfumu zaka khumi ndi
ziwiri. 2Nacita coipa pamaso pa Yehova, koma osati monga atate
wace ndi amace; pakuti anacotsa coimiritsa ca Baala adacipanga
atate wace. 3Koma anakangamira zoipa za Yerobiamu mwana wa
Nebati, zimene anacimwitsa nazo Israyeli, osalekana nazo.
4Ndipo Mesa mfumu ya Moabu anali mwini nkhosa, akapereka kwa
mfumu ya Israyeli ubweya wa ana a nkhosa zikwi zana limodzi, ndi
wa mphongo zikwi zana limodzi. 5Kama kunacitika, atafa Ahabu
mfumu ya Moabu anapandukana ndi mfumu ya Israyeli. 6Ndipo
mfumu Yehoramu anaturuka m'Samariya nthawi yomweyo,
namemeza Aisrayeli onse. 7Nakatumiza mau kwa Yehosafati
mfumu ya Yuda, ndi kuti, Mfumu ya Moabu wapandukana ndi ine;
kodi udzamuka nane kukathira nkhondo pa Moabu? Nati,
Ndidzakwera: ine ndikhala ngati iwe, anthu anga ngati anthu ako,
akavalo anga ngati akavalo ako. 8Ndipo anati, Tikwerere njira yiti?
Nati iye, Njira ya ku cipululu ca Edomu. 9Namuka mfu mu ya
Israyeli, ndi mfumu ya Yuda, ndi mfumu ya Edomu, nazungulira
njira ya masiku asanu ndi awiri; ndipo panalibe madzi kuti
ankhondo amwe, kapena nyama zakuwatsata. 10Ndipo mfumu ya
Israyeli inati, Kalanga ife! pakuti Yehova waitana mafumu ife atatu
kutipereka m'dzanja la Moabu. 11Koma Yehosafati anati, Palibe
pano mneneri wa Yehova kodi, kuti tifunsire Yehova mwa iye?
Ndipo wina wa anyamata a mfumu ya Israyeli anayankha, nati,
Elisa mwana wa Safati ali pano, ndiye uja anathira madzi m'manja
a Eliya. 12Nati Yehosafati, Mau a Yehova ali ndi iyeyo, Pamenepo
mfumu ya Israyeli, ndi Yehosafati, ndi mfumu ya Edomu, anatsikira
kuli iye. 13Ndipo Elisa anati kwamfumuya Israyeli, Ndiri ndi ciani
ndi inu? mukani kwa aneneri a atate wanu, ndi kwa aneneri a amai
wanu. Koma mfumu ya Israyeli inanena naye, Iai, pakuti Yehova
anaitana mafumu ife atatu kutipereka m'dzanja la Moabu. 14Ndipo
Elisa anati, Pali Yehova wa makamu, amene ndiima pamaso pace,
ndikadapanda kusamalira nkhope ya Yehosafati mfumu ya Yuda,
sindikadakuyang'anitsani, kapena kukuonani. 15Koma tsopano,
nditengereni wanthetemya. Ndipo kunali, waothetemyayo ali
ciyimbire, dzanja la Yehova linamgwera. 16Ndipo anati, Atero
Yehova, Kumbani m'cigwa muno mukhale maenje okha
okha. 17Pakuti atero Yehova, Simudzaona mphepo, kapena kuona
mvula, koma cigwaco cidzadzala ndi madzi; ndipo mudzamwa inu,
ndi ng'ombe zanu, ndi zoweta zanu. 18Ndipo ici cidzapepuka

pamaso pa Yehova; adzaperekanso Amoabu m'dzanja
lanu. 19Ndipo mudzakantha midzi yonse ya matioga, ndi midzi
yonse yosankhika, ndi kulikha mitengo yonse yabwino, ndi
kufotsera zitsime zonse zamadzi, ndi kuipitsa pa nthaka ponse
pabwino ndi miyala. 20Ndipo kunacitika m'mawa, pomapereka
nsembe yaufa, taonani, anafika madzi odzera ku Edomu; ndipo
dziko linadzala ndi madzi. 21Atamva tsono Amoabu onse kuti
adakwera mafumu aja kuthirana nao nkhondo, anamemeza onse
akumanga lamba m'cuuno ndi okulapo, naima iwo
m'malire. 22Ndipo pamene anauka mamawa dzuwa linawala
pamadzipo, naona Amoabu madzi ali pandunji pao ali psyu ngati
mwazi; 23nati, Uja ndi mwazi, atha kuonongana mafumu aja,
anakanthana wina ndi mnzace; ndipo tsopano, tiyeni Amoabu inu,
tikafunkhe. 24Ndipo pamene anafika ku misasa ya Israyeli, Aisrayeli
ananyamuka, nakantha Amoabu, nathawa iwo pamaso pao; ndipo
analowa m'dziko ndi kukantha Amoabu. 25Napasula midzi, naponya
yense mwala wace panthaka ponse pabwino, naidzaza, nafotsera
zitsime zonse zamadzi, nagwetsa mitengo yonse yabwino, kufikira
anasiya miyala yace m'Kirihasereti mokha; koma oponya miyala
anauzinga, naukantha. 26Ndipo ataona mfumu ya Moabu kuti
nkhondo idamlaka, anapita nao anthu mazana asanu ndi awiri
akusolola lupanga, kupyola kufikira kwa mfumu ya Edomu, koma
sanakhoza. 27Pamenepo anagwira mwana wace wamwamuna
woyamba amene akadakhala mfumu m'malo mwace, nampereka
nsembe yopsereza palinga. Ndipo anakwiyira Israyeli kwambiri;
potero anamcokera, nabwerera ku dziko lao.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Elisa afurukitsa mafuta a mkazi wamasiye

1Ndipo wina wa akazi a ana a aneneri anapfuula kwa Elisa, ndi kuti, Mnyamata wanu, mwamuna wanga wafa; mudziwa kuti mnyamata wanu anaopa Yehova; ndipo wafika wamangawa kunditengera ana anga awiri akhale akapolo ace. 2Ndipo Elisa anati kwa iye, Ndikucitire ciani? undiuze m'nyumba mwako muli ciani? Nati, Mdzakazi wanu alibe kanthu m'nyumba, koma mtsuko wa mafuta. 3Pamenepo anati, Kabwereke zotengera kwina kwa anansi ako onse, zotengera zopanda kanthu, zisakhale pang'ono. 4Nulowe, uudzitsekere wekha ndi ana ako amuna ndi kutsanulira m'zotengera zonsezi, nuike padera zodzalazo. 5Pamenepo anamcokera, nadzitsekera yekha ndi ana ace amuna; iwo namtengera zotengerazo, iye namatsanulira. 6Ndipo kunali, zitadzala zotengera, anati kwa mwana wace, Nditengere cotengera cina, Nanena naye, Palibe cotengera cina. Ndipo mafuta analeka. 7Pamenepo anadza, namfotokozera munthu wa Mulungu. Nati iye, Kagulitse mafuta, ukabwezere mangawa ako, ndi zotsalapo zikusunge iwe ndi ana ako.

Mkazi wa ku Sunemu ndi mwana wace

8Ndipo linafika tsiku lakuti Elisa anapitirira kumka ku Sunemu, kumeneko kunali mkazi womveka; ameneyo anamuumiriza adye mkate. Potero pomapitirako iyeyu, adafowapa, mbukirako kukadya mkate. 9Ndipo mkaziyo anati kwa mwamuna wace, Taona, tsopano ndidziwa kuti munthu uyu wakupitira pathu pano cipitire ndiye munthu woyera wa Mulungu. 10Timmangire kacipinda kosanja, timuikirenso komweko kama, ndi gome, ndi mpando, ndi coikapo nyali; ndipo kudzatero kuti akatidzera alowe m'mwemo. 11Ndipo linadza tsiku lakuti anafikako, nalowa m'cipinda cosanja, nagona komweko. 12Nati kwa Gehazi mnyamata wace, Itana Msunemu uja. Namuitana, naima mkaziyo pamaso pace. 13Ndipo anati kwa iye, Ufunse mkaziyu tsopano, kuti, Taona watisungira ndi kusamalira uku konse; nanga tikucitire iwe ciani? Kodi tikunenere kwa mfumu, kapena kwa kazembe wa nkhondo? Koma anati, Ndikhala ine pakati pa anthu a mtundu wanga. 14Pamenepo anati, Nanga timcitire iye ciani? Nati Gehazi, Zedi alibe mwana, ndi mwamuna wace wakalamba. 15Nati, Kamuitane. Namuitana, naima pakhomo mkaziyo. 16Ndipo anati, Nyengo yino caka cikudzaci udzafukata mwana wamwamuna. Koma anati, lai, mbuyanga, munthu wa Mulungu, musanamiza mdzakazi wanu. 17Ndipo mkaziyo anaima, naona mwana wamwamuna nyengo yomweyo caka cimene cija Elisa adanena naye. 18Ndipo atakula mwanayo, linadza tsiku lakuti anaturuka kumka kwa atate wace, ali kwa omweta

tirigu. 19Natikwa atate wace, Mutu wanga, mutu wanga! Pamenepo anati kwa mnyamata, Umnyamule umuke naye kwa amace. 20Namnyamula, napita naye kwa amace. Ndipo anakhala pa maondo ace kufikira usana, namwalira. 21Ndipo anakwera, namgoneka pa kama wa munthu wa Mulungu, naturuka, namtsekera. 22Naitana mwamuna wace, nati, Nditumizire mmodzi wa anyamata ndi buru mmodzi, kuti ndithamangire kwa munthu uja wa Mulungu, ndi kubweranso. 23Ndipo anati, Ulikumuka kwa iye lero cifukwa ninji? ngati mwezi wakhala, kapena: mpa sabata? Koma anati, Kuli bwino. 24Pamenepo anamangirira buru mbereko, nati kwa mnyamata wace, Kusa, tiye; usandilezetsa kuyendaku, ndikapanda kukuuza. 25Potero anamuka, nafika kwa munthu wa Mulungu ku phiri la Karimeli. Ndipo kunali, pakumuona munthu wa Mulungu alinkudza kutali, anati kwa Gehazi mnyamata wace, Tapenya, suyo Msunemu uja; 26uthamange tsopano kukomana naye, nunene naye, Muli bwino kodi? mwamuna wanu ali bwino? mwanayo ali bwino? Ndipo anati, Ali bwino. 27Ndipo pofika kwa munthu wa Mulungu kuphiri anamgwira mapazi. Ndipo Gehazi anayandikira kuti amkankhe; koma munthu wa Mulungu anati, Umleke, pakuti mtima wace ulikumwawa; ndipo Yehova wandibisira osandiuza ici. 28Ndipo mkaziyo anati, Ngati ndinapempha mwana kwa mbuyanga? Kodi sindinati, Musandinyenga? 29Pamenepo anati kwa Gehazi, Udzimangire m'cuuno, nutenge ndodo yanga m'dzanja lako, numuke; ukakomana ndi munthu usamlankhule; akakulankhula wina usamyankhe; ukaike ndodo yanga pankhope pa mwanayo. 30Koma mace wa mwana anati, Pali Yehova, pali inunso, ngati nkukusiyani. Ndipo ananyamuka, namtsata. 31Nawatsogolera Gehazi, naika ndodo pankhope pa mwanayo; koma mwanayo analibe mau, kapena kusamalira. Motero anabwerera kukomana naye, namuuza kuti, Sanauke mwanayo. 32Ndipo pamene Elisa analowa m'nyumba, taonani, mwanayo ngwakufa, adamgoneka pakama pace. 33Nalowa Elisa, nadzitsekera awiriwa, napemphera kwa Yehova. 34Nakwera, nagona pa mwanayo ndi kulinganiza pakamwa pace ndi pakamwa pace, maso ace ndi maso ace, zikhato zace ndi zikhato zace, nadzitambasula pa iye, ndi mnofu wa mwana unafunda. 35Pamenepo anabwera nayenda m'nyumba, cakuno kamodzi, cauko kamodzi; nakwera, nadzitambasuliranso pa iye; ndi mwana anayetsemula kasanu ndi kawiri, natsegula mwanayo maso ace. 36Pamenepo anaitana Gehazi, nati, Kaitane Msunemu uja, Namuitana. Ndipo atalowa kuli iye, anati, Nyamula mwana wako. 37Iye nalowa, nagwa pa mapazi ace, nadziweramitsa pansi; nanyamula mwana wace, naturuka.

Muli imfa m'nkhalimo

38Ndipo Elisa anabwera ku Giligala, koma m'dzikomo munali njala;
ndi ana a aneneri anali kukhala pansi pamaso pace; ndipo anati
kwa mnyamata wace, Ika nkhali yaikuruyo, uphikire ana a
aneneri. 39Naturuka wina kukachera ndiwo kuthengo, napeza
conga ngati mpesa, nacherapo zipuzi kudzaza m'pfunga mwace,
nadza, nazicekera-cekera m'nkhali ya cakudya, popeza
sanazidziwa. 40Pamenepo anagawira anthu kuti adye. Koma kunali;
pakudya cakudyaco, anapfuula nati, Munthu wa Mulungu, muli
imfa m'nkhalimo. Ndipo sanatha kudyako. 41Pamenepo anati,
Bwera naoni ufa. Nathira m'nkhalimo; nati, Gawirani anthu kuti
adye. Ndipo m'nkhalimo munalibe cowawa.

Mikate makumi awiri ikwanira anthu ambiri

42Ndipo anadza munthu kucokera ku Baala Salisa, nabwera nayo
mikate ya zipatso zoyamba kwa munthu wa Mulungu, mikate ya
barele makumi awiri, ndi ngala zaziwisi za tirigu zosaomba. Ndipo
anati, Uwapatse anthu kuti adye. 43Koma mnyamata wace anati,
Ciani? ndigawire amuna zana ici kodi? Koma anati, Uwapatse anthu
kuti adye; pakuti atero Yehova, Adzadya nadzasivako. 44Potero
anawagawira, nadya, nasiyapo, monga mwa mau a Yehova.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Namani wakhateyo aciritsidwa

1Ndipo Namani kazembe wa khamu la nkhondo la mfumu ya
Aramu anali munthu womveka pamaso pa mbuyace, ndi waulemu;
popeza mwa iye Yehova adapulumutsa Aaramu; ndiyenso ngwazi,
koma wakhate. 2Ndipo Aaramu adaturuka magulu magulu,
nabwera nalo m'ndende buthu locokera ku dziko la Israyeli,
natumikira mkazi wa Namani iyeyu, 3Nati uyu kwa mbuyace
wamkazi, Mbuye wanga akadakhala kwa mneneri ali m'Samariya,
akadamciritsa khate lace. 4Ndipo analowa wina, nauza mbuye
wace, kuti, Buthulo lofuma ku dziko la Israyeli lanena zakuti
zakuti. 5Pamenepo mfumu ya Aramu inati, Tiye, muka,
ndidzatumiza kalata kwa mfumu ya Israyeli. Pamenepo anacoka,
atatenga siliva: matalente khumi, ndi golidi masekeli zikwi zisanu
ndi cimodzi, ndi zobvala zakusintha khumi. 6Ndipo anafika kwa
mfumu ya Israyeli ndi kalata, wakuti, Pakulandira kalata uyu,
taonani, ndatumiza Namani mnyamata wanga kwa inu, kuti
mumciritse khate lace. 7Ndipo kunali atawerenga kalatayu mfumu
ya Israyeli, anang'amba zobvala zace, nati, Ngati ndine Mulungu,
kupha ndi kubwezera moyo, kuti ameneyo atumiza kwa ine
kumciritsa munthu khate lace? pakuti dziwani, nimupenye, kuti
alikufuna cifukwa pa ine. 8Koma kunali, pamene Elisa munthu wa
Mulungu anamva kuti mfumu ya Israyeli adang'amba zobvala zace,
anatumiza mau kwa mfumu, ndi kuti, Mwang'amba zobvala zanu
cifukwa ninji? Adzetu kwa ine, ndipo adzadziwa kuti muli mneneri
m'Israyeli. 9M'mwemo: Namani anadza ndi akavalo ace ndi
magareta ace, naima pakhomo pa nyumba ya Elisa. 10Ndipo Elisa
anamtumira mthenga, ndi kuti, Kasambe m'Yordano kasanu ndi
kawiri, ndi mnofu wako udzabwerera momwe, nudzakhala
wokonzeka. 11Koma Namani adapsa mtima, nacoka, nati, Taona,
ndinati m'mtima mwanga, kuturuka adzanditurukira, nadzaima ndi
kuitana pa dzina la Yehova Mulungu wace, ndi kuweyula dzanja
lace pamalopo, ndi kuciritsa wakhateyo. 12Nanga Abana ndi
Faripara, mitsinje ya Damasiko, siiposa kodi madzi onse a
m'Israyeli? ndilekerenji kukasamba m'mwemo, ndi kukonzeka?
Natembenuka, nacoka morunda. 13Pamenepo anyamata ace
anasendera, nanena naye, nati, Atate wanga, mneneri
akadakuuzani cinthu cacikuru, simukadacicita kodi? koposa kotani
nanga ponena iye, Samba, nukonzeke? 14Potero anatsika, namira
m'Yordano kasanu ndi kawiri, monga adanena munthu wa
Mulunguyo; ndi mnofu wace unabwera monga mnofu wa mwana
wamng'ono, nakonzeka. 15Pamer nepo anabwerera kwa munthu
wa Mulungu iye ndi gulu lace lonse, nadzaima pamaso pace, nati,
Taonani, tsopano ndidziwa kuti palibe Mulungu pa dziko lonse

lapansi, koma kwa Israyeli ndiko; ndipo tsopano, mulandire cakukuyamikani naco kwa mnyamata wanu. 16Koma anati, Pali Yehova, amene ndiima pamaso pace, sindidzalandira kanthu. Ndipo anamkangamiza acilandire, koma anakana. 17Ndipo Namani anati, Mukakana, andipatse akatundu a dothi osenza nyuru ziwiri; pakuti mnyamata wanu sadzaperekanso nsembe yopsereza kapena yophera kwa milungu yina, koma kwa Yehova. 18Yehova akhululukire mnyamata wanu mwa ici; akalowa mbuye wanga m'nyumba ya Rimoni kulambiramo, nakatsamira pa dzanja langa, nanenso ndikagwadira m'nyumba ya Rimoni, pakugwadira ine m'nyumba ya Rimoni, Yehova akhululukire mnyamata wanu mwa ici. 19Ndipo ananena naye, Pita mumtendere. Ndipo anacoka, nayenda kanthawi.

Gehazi alangidwa ndi khate

20Koma Gehazi, mnyamata wa Elisa, munthu wa Mulungu, anati, Taona, mbuye wanga analekera Namani uyu wa ku Aramu osalandira m'manja ace cimene anabwera naco; pali Yehova, ndidzathamangira ndi kulandira kanthu kwa iye. 21Motero Gehazi anatsata Namani. Ndipo pamene Namani anaona wina alikumthamangira, anatsika pagareta kukomana naye, nati, Nkwabwino kodi? 22Nati, Kuli bwino. Mbuye wanga wandituma, ndi kuti, Taonani, andifikira tsopano apa anyamata awiri a ana a aneneri, ocokera ku mapiri a Efraimu; muwapatse talente wa siliva, ndi zobvala zosintha ziwiri. 23Nati Namani, Viole ulandire matalente awiri. Namkangamiza namanga matalente awiri a siliva m'matumba awiri, ndi zobvala zosintha ziwiri, nasenzetsa anyamata ace awiri; iwo anatsogola atazisenza. 24Ndipo pamene anafika kumsanje anazilandira m'manjamwao, naziika m'nyumba; nauza anthuwo amuke, iwo nacoka. 25Pamenepo analowa, na, ima kwa mbuye wace. Ndipo Elisa ananena naye, Ufuma kuti Gehazi? Nati, Ngati mnyamata wanu wayenda konse? 26Ndipo anati kwa iye, Mtima wanga sunakuperekeza kodi, umo munthuyo anatembenuka pa gareta wace kukomana ndi iwe? Kodi nyengo yino ndiyo yakulandira siliva, ndi kulandira zobvala, ndi minda yaazitona, ndi yampesa, ndi nkhosa, ndi ng'ombe, ndi akapolo; ndi adzakazi? 27Cifukwa cace khate la Namani lidzakumamatira iwe ndi mbumba yako cikhalire. Ndipo anaturuka pamaso pace wakhate wa mbu ngati cipale cofewa.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Elisa ayandamitsa citsulo pamadzi

1Ndipo ana a aneneri anati kwa Elisa, Taonani tsono, pamalo
tikhalapo ife pamaso panu paticepera 2Mutilole tipite ku Yordano,
tikatengeko, ali yense mtengo, tidzimangire malo komweko,
tikhalepo, Nati, Mukani. 3Ndipo wina anati, Mulole mupite nafe
anyamata anu. Nati, Ndidzamuka. 4Namuka nao, nafika ku
Yordano, iwo natema mitengo. 5Ndipo wina analinkudula mtengo
nkhwangwa inagwa m'madzi; ndipo anapfuula, nati, Kalanga ine
mbuyanga! popeza ojobwereka. 6Nati munthu wa Mulungu,
Yagwera pati? Namuonetsapo yagwera. Pamenepo anadula
kamtengo, nakaponya pomwepo, nayandamitsa
nkhwangwayo. 7Nati, Katole. Natambasula dzanja lace, naitenga.

Aaramu alangidwa ndi khungu ku Dotana

8Ndipo mfumu ya Aramu inalinkucita nkhondo ndi Israyeli,
nipangana ndi anyamata ace, kuti, Misasa yanga idzakhala pakuti
pakuti. 9Ndipo munthu wa Mulunguyo anatuma mau kwa mfumu
ya Israyeli, ndi kuti, Mucenjere musapite pakuti, popeza Aaramu
alikutsikira uko. 10Pamenepo mfumu ya Israyeli inatumiza kumene
munthu wa Mulungu anamuuzako ndi kumcenjeza; nadzisunga
osapitako, kawiri kawiri. 11Koma mtima wa mfumu ya Aramu
unabvutika kwambiri pa icico, naitana anyamata ace, nanena nao,
Kodi simudzandiuza wina wa ife wobvomerezana ndi mfumu ya
Israyeli ndani? 12Nati mmodzi wa anyamata ace, lai, mbuye wanga
mfumu; koma Elisa, mneneriyo ali ku Israyeli, ndiye amafotokozera
mfumu ya Israyeli mau muwanena m'kati mwace mwa cipinda
canu cogonamo. 13Nati iye, Kamuoneni komwe ali; ndikatume
munthu kumtenga. Ndipo anamuuza kuti, Ali ku
Dotana. 14Pamenepo anatumizako akavalo ndi magareta ndi
khamu lalikuru, nafikako usiku, nauzinga mudziwo. 15Ndipo
atalawirira mamawa mnyamata wa munthu wa Mulungu, naturuka,
taonani, khamu la nkhondo linazinga mudzi ndi akavalo ndi
magareta. Ndi mnyamata wace ananena naye, Kalanga ine, mbuye
wanga! ticitenji? 16Nati iye, Usaopa, pakuti okhala pamodzi ndi ife
acuruka koposa aja okhala pamodzi ndi iwo. 17Ndipo Elisa
anapemphera, nati, Yehova, mumtsegulire maso ace kuti aone.
Pamenepo Yehova anamtsegulira maso mnyamatayo, napenya iye,
ndipo taonani, paphiripo panadzala ndi akavalo ndi magareta
amoto akumzinga Elisa. 18Ndipo atatsikira pali iye, Elisa
anapemphera kwa Yehova, nati, Mukanthe mtundu uwu ucite
khungu. Ndipo iye anawakantha, nawacititsa khungu, monga mwa
mau a Elisa. 19Ndipo Elisa ananena nao, Ngati njira ndi iyi? ngati
mudzi ndi uwu? munditsate ine, ndidzakufikitsani kwa munthu
mumfunayo; nawatsogolera ku Samariya. 20Ndipo kunali, pakufika

ku Samariya, Elisa anati, Yehova, muwakanganulire awa maso kuti aone. Nawakanganulira Yehova maso ao, naona iwo, ndipo tapenyani, ali pakati pa Samariya. 21Niti mfumu ya Israyeli kwa Elisa pakuwaona, Atate wanga ndiwakanthe kodi, ndiwakanthe? 22Nati, Musawakanthe; kodi mumakantha omwe mwawagwira ndi lupanga ndi uta wanu? apatseni mkate ndi madzi adye namwe, namuke kwa mbuye wao. 23Ndipo anwakonzera cakudya cambiri, nadya namwa iwo; nawauza amuke; namuka kwa mbuye wao. Ndipo magulu a Aramu sanadzanso ku dziko la Israyeli.

Aaramu amangira Samariya misasa

24Ndipo zitatha izi, Benihadadi mfumu ya Aramu anamemeza khamu lace lonse, nakwera, namangira misasa Samariya. 25Koma m'Samariya munali njala yaikuru; ndipo taonani, anaumangira misasa mpaka mutu wa buru unagulidwa ndalama zasiliva makumi asanu ndi atatu; ndi limodzi la magawo anai la muyeso wa zitosi za nkhunda linagulidwa ndi ndalama zasiliva zisanu. 26Ndipo popita mfumu ya Israyeli alikuyenda palinga, mkazi anampfuulira, nati, Ndithandizeni, mbuye wanga mfumu. 27Nati iye, Akapanda kukuthandiza Yehova, ndikaona kuti kokuthandiza ine? kudwale kodi, kapena popondera mphesa 28Nanena naye mfumu, Ufunanji? Nati iye, Mnzanga uyu ananena ndi ine, Tenga mwana wako timudye lero, ndi mwana wanga timudye mawa. 29Ndipo tinaphika mwana wanga ndi kumudya, ndi mawa wace ndinanena naye, Tenga mwana wako, timudye; koma wambisa mwana wace. 30Ndipo pakumva mfumu mau a mkaziyo, anang'amba zobvala zace alinkupita nayenda palinga, anthu napenya; ndipo taonani, pali ciguduli m'kati pa thupi lace. 31Nati iye, Andilange Mulungu naonjezeko, ngati mutu wa Elisa mwana wa Safati uti ukhale pa iye lero lino.

Elisa aneneratu za cakudya cocuruka

32Koma Elisa anakhala pansi m'nyumba mwace, ndi akulu anakhala pansi pamodzi naye; ndipo mfumu inatuma munthu amtsogolere, koma asanafike kwa Elisa mthengayo, anati kwa akulu, Mwapenya kodi m'mene mwana uyu wambanda watumiza munthu kucotsa mutu wanga? taonani, pakufika mthengayo mutseke pakhomo, mumkankhe ndi citseko. Kodi mapazi a mbuye wace samveka dididi pambuyo pace? 33Akali cilankhulire nao, tapenyani, wamtsikira mthengayo; ndi mfumu inati, Taonani, coipa ici cicokera kwa Yehova; ndilindiranjinso Yehova?

©The Bible Society of Malawi, 1992

1Ndipo Elisa anati, Mverani mau; a Yehova; atero Yehova, Mawa
dzuwa lino adzagula muyeso wa ufa ndi sekeli, adzagulanso miyeso
iwiri ya barele ndi sekeli, pa cipata ca Samariya. 2Pamenepo
kazembe amene mfumu adafotsamira pa dzanja lace anamyankha
munthu wa Mulungu, nati, Taonani, Yehova angacite mazenera
m'mwamba cidzacitika ici kodi? Nati iye, Taona, udzaciona ndi maso
ako, koma iwe sudzadyako ai.

Akhate anai aulula za kuthawa Aaramu

3Koma polowera pa cipata panali amuna anai akhate, nanenana
wma ndi mnzace, Tikhaliranji kuno mpaka kufa? 4Tikati, Tilowe
m'mudzi, m'mudzi muli njala, tidzafa m'mwemo; tikakhala
pompano, tidzafanso. Tiyeni tsono, tigwe ku misasa ya Aaramu;
akatisunga ndi moyo, tidzakhala ndi moyo; akatipha,
tangokufa. 5Nanyamuka iwo kuli sisiro kukalowa ku misasa ya
Aaramu; koma pofika polekezera pace pa misasa ya Aaramu,
taonani, panalibe munthu pomwepo. 6Popeza Yehova adamvetsa
khamu la Aaramu phokoso la magareta ndi mkokomo wa akavalo,
phokoso la nkhondo yaikuru; nanenana wina ndi mnzace, Taonani
mfumu ya Israyeli watimemezera mafumu a Ahiti ndi mafumu a
Aaigupto, atigwere. 7Nanyamuka, nathawa kuli sisiro, nasiya
mahema ao, ndi akavalo ao, ndi aburu ao, misasa iri cimangire;
nathawa, apulumutse moyo wao. 8Ndipo pofika akhate ao
polekezera pa misasa, analowa m'hema mmodzi, nadya namwa,
natengako siliva ndi golidi ndi zobvala, namuka, nazibisa;
nabwerera, nalowa m'hema mwina, natengako, namuka,
nazibisa. 9Pamenepo ananenana wina ndi mnzace, Sitirikucita
bwino ife; tsiku lino ndilo tsiku la uthenga wabwino, ndipo
tirikukhala cete; tikacedwa kufikira kwaca, mphulupulu yathu
idzatipeza; tiyeni tsono, timuke, tifotokozere a m'nyumba ya
mfumu. 10Nadza iwo, naitana mlonda wa mudzi, namfotokozera;
ndi kuti, Tinafika ku misasa ya Aaramu, ndipo taonani, palibe
munthu pomwepo, kapena mau a munthu, koma akavalo omanga,
ndi aburu omanga, ndi mahema ali cimangire. 11Ndipo iye
anaitana alonda ena, ndi iwo anafotokozera a m'nyumba ya
mfumu. 12Niuka mfumu usiku, ninena ndi anyamata ace,
Ndikufotokozereni m'mene Aaramu aticitira ife. Adziwa kuti
tagwidwa ndi njala, laturuka m'misasa, nabisala kuurengo, ndi kuti,
Pamene aturuka m'mudzi tidzawagwira ndi moyo ndi kulowa
m'mudzimo. 13Nayankha mmodzi wa anyamata ace, nati, Atenge
tsono akavalo otsala asanu, ndiwo otsala m'mudzi; taonani,
adzanga unyinji wonse wa Israyeli otsalawo, kapena adzanga
unyinji wonse wa Israyeli otsirizika; tiwatumize tione. 14Motero
anatenga magareta awiri ndi akavalo ao; ndipo mfumu

inawatumiza alondole khamu la Aaramu, ndi kuti, Mukani mukaone. 15Ndipo anawalondola mpaka ku Yordano; ndipo taonani, m'njira monse munadzala ndi zobvala ndi akatundu adazitaya Aaramu m'kufulumira kwao. Nibwera mithenga, nifotokozera mfumu. 16Naturuka anthu, nafunkha m'misasa ya Aaramu. Ndipo anagula miyeso wa ufa ndi sekeli, nagulanso miyeso iwiri ya barele ndi sekeli, monga umo adanenera Yehova. 17Koma mfumu idayang'anitsa pacipata kazembe amene uja idafotsamira pa dzanja lace; ndipo anthu anampondereza pacipata, nafa iye, monga umo adanenera munthu wa Mulungu, ponena paja anamtsikira mfumu. 18Ndipo kunacitika, monga adanena munthu wa Mulungu kwa mfumu, ndi kuti, Adzagula miyeso iwiri ya barele ndi sekeli, adzagulanso muyeso wa ufa ndi sekeli; kudzatero mawa, dzuwa lino, pa cipata ca Samariya; 19ndipo kazembe uja adayankha munthu wa Mulunguyo, nati, Taonani tsono, Yehova angacite mazenera m'mwamba, cikacitika ici kodi? Nati iye, Taona, udzaciona ici ndi maso ako, koma osadyako ai; 20kudamcitikira momwemo; popeza anthu anampondereza pacipata nafa iye.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Wa ku Sunemu abwera kwao itatha njalayo

1Ndipo Elisa ananena ndi mkazi uja adamuukitsira mwana wace,
kuti, Nyamuka, numuke iwe ndi banja lako, nugonere komwe
ukaone malo; pakuti Yehova waitana njala, nidzagwera dziko zaka
zisanu ndi ziwiri. 2Nanyamuka mkaziyo, nacita monga mwa mau a
munthu wa Mulunguyo, namuka ndi banja lace, nagonera m'dziko
la Afilisti zaka zisanu ndi ziwiri. 3Ndipo pakutha pace pa zaka
zisanu ndi ziwirizo, mkaziyo anabwera kucoka m'dziko la Afilisti,
naturuka kukanena za nyumba yace ndi munda wace kwa
mfumu. 4Koma mfumu inalikulankhula ndi Gehazi mnyamata wa
munthu wa Mulungu, ndi kuti, Ndifotokozere zazikuru zonse Elisa
wazicita. 5Ndipo kunali, alimkufotokozera mfumu m'mene
adamuukitsira wakufayo, taonani, mkaziyo adamuukitisira mwana
wace ananena za nyumba yace ndi munda wace kwa mfumu. Nati
Gehazi, Mbuye wanga mfumu, suyu mkaziyo, suyu mwana wace
Elisa anamuukitsayo? 6Ndipo pofunsa mfumu, mkaziyo
anaisimbira. Pamenepo mfumu anamuikira mdindo, ndi kuti,
Bwezetsa zace zonse ndi zipatso zonse za m'munda, cicokere iye
m'dziko mpaka lero lino.

Hazaeli mfumu ya Aramu

7Ndipo Elisa anafika ku Damasiko, podwala Benihadadi mfumu ya
Aramu; ndipo anamuuza, kuti, Munthu wa Mulungu wadza
kuno. 8Niti mfumu kwa Hazaeli, Tenga caufulu m'dzanja lako,
nukamkumike munthu wa Mulungu, nukafunsire Yehova mwa iye,
ndi kuti, Ndidzacira kodi nthenda iyi? 9Namuka Hazaeli
kukakomana naye, napita naco caufulu, ndico ca zokoma zonse za
m'Damasiko, zosenza ngamila makumi anai, nafika naima pamaso
pace, nati, Mwana wanu Benihadadi mfumu ya Aramu, wandituma
ine kwa inu, ndi kuti, Kodi ndidzacira nthenda iyi? 10Nanena naye
Elisa, Kamuuze, kuti, Sudzacira konse; popeza Yehova wandionetsa
kuti adzafa ndithu. 11Ndipo anamyang'ana cidwi, mpaka anacita
manyazi, nalira misozi munthu wa Mulungu. 12Nati Hazaeli,
Muliriranji, mbuye wanga? Nayankha iye, Popeza ndidziwa coipa
udzacitira ana a Israyeli; udzatentha malinga ao ndi moto,
nudzapha anyamata ao ndi lupanga, nudzaphwanya makanda ao,
nudzang'amba akazi ao okhala ndi pakati. 13Nati Hazaeli, Koma
nanga kapolo wanu ali ciani, ndiye garu, kuti akacite cinthu
cacikuru ici? Nayankha Elisa, Yehova wandionetsa kuti udzakhala
mfumu ya pa Aramu. 14Ndipo anacoka kwa Elisa, nadza kwa
mbuye wace; ameneyo ananena naye, Anakuuza ciani Elisa? Nati
iye, Anandiuza kuti mudzacira ndithu. 15Ndipo kunali m'mawa
mwace, anatenga cimbwi, nacibviika m'madzi, naciphimba

pankhope pa mfumu, nifa; ndipo Hazaeli analowa ufumu m'malo mwace.

Yehoramu mfumu ya Yuda

16Ndipo caka cacisanu ca Yoramu mwana wa Ahabu mfumu ya Israyeli, pokhala Yehosafati mfumu ya Yuda, Yehoramu mwana wa Yehosafati analowa ufumu. 17Ndiye wa zaka makumi atatu ndi ciwiri polowa ufumu wace, nacita ufumu zaka zisanu ndi zitatu ku Yerusalemu. 18Nayenda m'njira ya mafumu a Israyeli, m'mene inacitira nyumba ya Ahabu; pakuti mkazi wace ndiye mwana wa Ahabu, nacita iye coipa pamaso pa Yehova. 19Koma Yehova sanafuna kuononga Yuda, cifukwa ca Davide mtumiki wace monga adamuuza, kuti adzampatsa nyali ya kwa ana ace kosalekeza. 20Masiku ace Aedomu anapanduka ku ulamuliro wa Yuda, nadziikira mfumu okha. 21Pamenepo Yoramu anaoloka kumka ku Zairi, ndi magareta ace onse pamodzi naye; nauka iye usiku, nakantha Aedomu akumzinga ndi nduna za magareta, nathawira anthu ku mahema ao. 22Motero Aedomu anapanduka ku ulamuliro wa Yuda mpaka lero lino. Ndipo Alibina anapanduka nthawi yomweyi. 23Ndi macitidwe ena a Yoramu, ndi zonse anazicita, sizinalembedwa kodi m'buku la macitidwe a mafumu a Yuda. 24Nagona Yoramu ndi makolo ace, naikidwa pamodzi ndi makolo ace m'mudzi wa Davide; ndipo Ahaziya mwana wace anakhala mfumu m'malo mwace.

Ahaziva mfumu ya Yuda

25Caka cakhumi ndi ziwiri ca Yoramu mwana wa Ahabu mfumu Ahaziya mwana wa Yehoramu mfumu ya Yuda analowa ufumu wace. 26Ahaziya ndiye, Wa zaka makumi awiri mphambu ziwiri polowa ufumu wace, nakhala mfumu m'Yerusalemu caka cimodzi. Ndi dzina la mace ndiye Ataliya mdzukulu wa Omri mfumu ya Israyeli. 27Ndipo anayenda m'njira ya nyumba ya Ahabu, nacita coipa pamaso pa Yehova, m'mene inacitira nyumba ya Ahabu; pakuti ndiye wa cibale ca banja la Ahabu. 28Ndipo anamuka Yoramu mwana wa Ahabu kukathira nkhondo pa Hazaeli mfumu ya Aramu ku Ramoti Gileadi; ndi Aaramu analasa Yoramu. 29Ndipo mfumu Yoramu anabwera kuti ampoletse m'Yezreeli mabalawo adamkantha Aaramu ku Rama, polimbana naye Hazaeli mfumu ya Aramu, Natsikirako Ahaziya mwana wa Yehoramu mfumu ya Yuda kukamuona Yoramu mwana wa Ahabu m'Yezreeli, pakuti anadwala.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Yehu adzozedwa mfumu ya Israyeli

1Ndipo Elisa mneneriyo anaitana mmodzi wa ana a aneneri,
nanena naye, Udzimangire m'cuuno, nutenge nsupa iyi ya mafuta
m'dzanja mwako, numuke ku Ramoti Gileadi. 2Ndipo ukafikako,
ukaunguzeko Yehu mwana wa Yehosafati mwana wa Nimsi, nulowe
numnyamukitse pakati pa abale ace, nupite naye ku cipinda
cam'katimo. 3Nutenge nsupa ya mafutayo, nuwatsanulire pamutu
pace, nunene, Atero Yehova; Ndakudzoza iwe ukhale mfumu pa
Israyeli. Utatero, tsegula pakhomo, nuthawe
osacedwa, 4Pamenepo mnyamatayo, ndiye mneneri, anamuka ku
Ramoti Gileadi. 5Nalowa, ndipo taonani, akazembe a khamu
alikukhala pansi; nati iye, Ndiri ndi mau kwa inu, kazembe. Nati
Yehu, Kwa yani wa ife tonse? Nati iye, Kwa Inu,
kazembe. 6Nanyamuka, nalowa m'nyumba; ndipo anatsanulira
mafutawo pamutu pace, nanena naye, Atero Yehova Mulungu wa
Israyeli, Ndakudzoza ukhale mfumu ya pa anthu a Yehova, ndiwo
Aisrayeli. 7Nudzakantha nyumba ya Ahabu mbuye wako, kuti
ndibwezere cilango ca mwazi wa: atumiki anga aneneri, ndi mwazi
wa atumiki onse a Yehova, dzanja la Yezebeli. 8Popeza nyumba
yonse ya Ahabu idzaonongeka, ndipo ndidzalikhira Ahabu ana
amuna onse womangika ndi womasuka m'Israyeli. 9Ndipo
ndidzalinganiza nyumba ya Ahabu ndi nyumba ya Yerobiamu
mwana wa Nebati, ndi nyumba ya Basa mwana wa Ahiya. 10Ndipo
agaru adzamudya Yezebeli pa dera la Yezreeli, wopanda wina
wakumuika. Pamenepo anatsegula pakhomo, nathawa. 11Ndipo
Yehu anaturukira kwa anyamata a mbuye wace, nanena naye
wina, Mtendere kodi? anakudzera cifukwa ninji wamisala uyu?
Nanena nao, Mumdziwa munthuyo ndi makambidwe ace. 12Nati
iwo, Kunama uku; utifotokozere tsono. Nati iye, Anati kwa ine
cakuti cakuti; ndi kuti, Atero Yehova, Ndakudzoza mfumu pa
Israyeli. 13Nafulumira iwo, nagwira yense copfunda cace, naciyala
pokhala iye paciunda, naomba lipenga, nati, Yehu ndiye mfumu.

Yehu awapha Yoramu ndi Ahaziya

14Motero Yehu mwana wa Yehosafati mwana wa Nimsi
anapandukira Yoramu. Tsono Yoramu atalindira ku Ramoti Gileadi,
iye ndi Aisrayeli onse, cifukwa ca Hazaeli mfumu ya
Aramu; 15koma mfumu Yoramu adabwera ku Yezreeh ampoletse
mabala ace anamkantha Aaramu, muja adalimbana naye Hazaeli
mfumu ya Aramu. Nati Yehu, Ukatero mtima wanu, asapulumuke
mmodzi yense kuturuka m'mudzi kukafotokozera
m'Yezreeli. 16Nayenda Yehu m'gareta, namuka ku Yezreeli, popeza
Yoramu anagonako; ndi Ahaziya mfumu ya Yuda anatsikira
kukamuona Yoramu. 17Ndipo mlonda ali ciriri pacilindiro m'Yezreeli,

naona gulu la Yehu lirinkudza, nati, Ndiona gulu. Nati Yoramu, Tenga wapakavalo, numtumize akomane nao, nanene, Mtendere kodi? 18Ndipo anamuka wapakavalo kukomana naye, nati, Atero mfumu, Mtendere kodi? Nati Yehu, Ngwanji mtendere, tembenukira m'mbuyo mwanga. Ndi mlonda anawafotokozera kuti, Mthenga wawafika, koma wosabwera. 19Pamenepo anatumiza wina wapakavalo, nawafika, nati, Atero mfumu, Mtendere kodi? Nati Yehu, Ngwanji mtendere, tembenukira m'mbuyo mwanga. 20Ndi mlonda anafotokozera, kuti, Wawafika, koma wosabwera; ndipo kuyendetsako kukunga kuyendetsa kwa Yehu mwana wa Nimsi, pakuti ayendetsa moyaruka. 21Nati Yoramu, Manga. Namanga gareta wace, Ndipo Yoramu mfumu ya Israyeli ndi Ahaziya mfumu ya Yuda anaturuka yense m'gareta wace, naturuka kukakomana ndi Yehu, nakomana naye pa munda wa Naboti m'Yezreeli. 22Ndipo kunali, pamene Yoramu anaona Yehu, anari, Mtendere kodi, Yehu? Nati iye, Ngwanji mtendere pokhala cacuruka cigololo ndi nyanga zace za mai wako Yezebeli? 23Natembenuza Yoramu manja ace, nathawa, nati kwa Ahaziya, Ciwembu, Ahaziya. 24Nafa nao Yehu uta wace, nalasa Yoramu pacikota, nuturuka mubvi pa mtima wace, naonyezeka iye m'gareta wace. 25Nati Yehu kwa Bidikara kazembe wace, Mnyamule, numponye m'munda wa Naboti wa ku Yezreeli; pakuti kumbukila m'mene ine ndi iwe tinali pa akavalo athu pamodzi kutsata Ahabu atate wace, Yehova anamsenzetsa katundu uyu. 26Ndapenyadi dzulo mwazi wa Naboti ndi mwazi wa ana ace, ati Yehova; ndipo ndikubwezera pamunda pano, ati Yehova, Mtengeni tsono, mumponye pamundapo, monga mwa mau a Yehova. 27Koma pociona ici Ahaziya mfumu ya Yuda anathawa njira ya ku khumbi la m'munda. Namtsata Yehu, nati, Mumkanthe uyonso pagareta; namkantha pa cikweza ca Guru ciri pafupi pa Yibleamu. Nathawira iye ku Megido, namwalira komweko. 28Ndipo anyamata ace anamnyamulira pagareta kumka naye ku Yerusalemu, namuika ku manda ace pamodzi ndi makolo ace m'mudzi wa Davide.
29Ndipo pa caka cakhumi ndi cimodzi ca Yoramu mwana wa Ahabu, Ahaziya analowa ufumu pa Yuda.

Imfa ya Yezebeli

30Ndipo pofika Yehu ku Yezreeli, Yezebeli anamva, nadzikometsera m'maso, naluka tsitsi lace, nasuzumira pazenera. 31Ndipo polowa Yehu pacipata, mkaziyo anati, Mtendere kodi Zimri, iwe wakupha mbuyako? 32Koma anakweza maso ace kuzenera, nati, Ali ndi ine ndani? Ndani? Nampenyererako adindo awiri kapena atatu. 33Nati iye, Mgwetsereni pansi. Namgwetsera pansi, nuwazikako mwazi wace pakhoma ndi pa akavalo, nampondereza iye pansi. 34Ndipo atalowa, anadya namwa, nati, Kampenyeni tsono mkazi

wotembereredwa uyu, nimumuike; popeza ndiye mwana wa mfumu. 35Namuka iwo kuti amuike; koma sanapezako kanthu kena koma bade, ndi mapazi, ndi zikhato za manja. 36Nabwerera iwo, namfotokozera. Nati iye, Ndiwo mau a Yehova ananena wo mwa mtumiki wace Eliya wa ku Tisibe, ndi koti, Pa munda wa Yezreeli agaru adzadya mnofu wa Yezebeli; 37ndi thupi la Yezebeli lidzakhala ngati ndowe pamunda m'dera la Yezreeli, kuti sadzati, Ndi Yezebeli uyu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Yehu aononga mbumba ya Ahabu

1Ndipo Ahabu anali nao ana amuna makumi asanu ndi awiri
m'Samariya. Nalemba akalata Yehu, natumiza ku Samariya kwa
akulu a Yezreeli, ndiwo akulu akulu, ndi iwo adalera ana a Ahabu,
ndi kuti, 2Tsono akakufikani inu kalata uyu, popeza muli nao ana a
mbuye wanu; muli naonso magareta ndi akavalo, ndi mudzi
walinga, ndi zida, 3musankhe wokoma ndi woyenerayo wa ana a
mbuye wanu, ndi kumuika pa mpando wacifumu wa atate wace;
ndipo muiponyere nkhondo nyumba ya mbuye wanu. 4Koma
anaopa kwambiri, nati, Taonani, mafumu awiri sanaima pamaso
pace, nanga ife tidzaima bwanji? 5Ndipo iye wakuyang'anira
nyumba, ndi iye wakuyang'anira mudzi, ndi akulu akulu, ndi iwo
akulera anawo, anatumiza kwa Yehu, ndi kuti, Ife ndife akapolo anu
ndi zonse mutiuza tidzacita; sitidzalonga munthu yense mfumu;
cokomera pamaso panu citani. 6Nawalembera kalata kaciwiri, nati,
Mukakhala a ine ndi kumvera mau anga, tengani mitu va amunawo
ana a mbuyewanu, ndi kundidzera ku Yezreeli mawa dzuwa lino.
Koma ana a mfumu ndiwo amuna makumi asanu ndi awiri,
anakhala ndi anthu omveka m'mudzi, amene anawalera. 7Ndipo
kunali, powafika kalatayo, anatenga ana a mfumu, nawapha
amuna makumi asanu ndi awiri, naika mitu yao m'mitanga,
naitumiza kwa iye ku Yezreeli. 8Nudza mthenga, numfotokozera,
kuti, Abwera nayo mitu va ana a mfumu. Nati iye, Mulunjike miulu
iwiri polowera pa cipata kufikira m'mawa. 9Ndipo kunali m'ma wa,
iye anaturuka, naima, nati kwa anthu onse, Muli olungama inu,
taonani, ndinapandukira mbuye wanga ndi kumupha; koma awa
onse anawakantha ndani? 10Dziwani tsono, kuti sikadzagwa pansi
kanthu ka mau a Yehova, amene Yehova ananena za nyumba va
Ahabu; pakuti Yehova wacita cimene adanena mwa mtumiki wace
Eliya. 11Nawakantha Yehu otsala onse a nyumba ya Ahabu
m'Yezreeli, ndi omveka ace onse, ndi odziwana naye, ndi ansembe
ace, mpaka sanatsala wa iye ndi mmodzi yense. 12Pamenepo
ananyamuka, nacoka, namuka ku Samariya, Ndipo pokhala ku
nyumba yosengera ya abusa panjira, 13Yehu anakomana nao abale
a Ahaziya mfumu ya Yuda, nati, Ndinu ayani? Nati iwo, Ife ndife
abale a Ahaziya, tirikutsika kulankhulira ana a mfumu, ndi ana a
nyumba yaikuru. 14Nati iye, Agwireni amoyo. Nawagwira amoyo,
nawapha ku dzenje la nyumba yosengera, ndiwo amuna makumi
anai mphambu awiri; sanasiya ndi mmodzi yense.

Aphedwa aneneri a Baala

15Atacoka pamenepo, anakomana naye Yehonadabu mwana wa
Rekabu wakudzamcingamira; namlankhula, nanena naye, Mtima
wako ngwoongoka kodi, monga mtima wanga ubvomerezana nao

mtima wako? Nati Yehonadabu, Momwemo. Ukatero undipatse dzanja lako. Nampatsa dzanja lace, namkweretsa pali iye pagareta. 16Nati iye, Tiye nane, ukaone cangu canga ca kwa Yehova. M'mwemo anamuyendetsa m'gareta wace. 17Ndipo anafika ku Samariya, nakantha onse otsala a Ahabu m'Samariya, mpaka adamuononga monga mwa mau a Yehova adanenawo kwa Elisa. 18Ndipo Yehu anasonkhanitsa anthu onse pamodzi, nanena nao, Ahabu anatumikira Baala pang'ono, koma Yehu adzamtumikira kwambiri. 19Mundiitanire tsono adze kwa ine aneneri onse a Baala, ompembedza onse, ndi ansembe ace onse, asasowe mmodzi; pakuti ndiri nayo nsembe yaikuru yocitira Baala; ali yense wosapenyekapo sadzakhala ndi moyo. Kama Yehu anacicita monyenga, kuti akaononge otumikira Baala. 20Nati Yehu, Lalikirani msonkhano wopatulika wa Baala. Naulalikira. 21Ndipo Yehu anatumiza kwa Aisrayeti onse, nadza otumikira Baala onse, wosatsala ndi mmodzi yense wosafika. Nalowa m'nyumba ya Baala; ndi nyumba ya Baala inadzala pha. 22Nati kwa iye wosunga nyumba ya zobvala, Turutsira otumikira Baala onse zobvala. Nawaturutsira zobvala. 23Nalowa Yehu ndi Yehonadabu mwana wa Rekabu m'nyumba ya Baala, nati kwa otumikira Baala, Mufunefune, nimuone asakhale nanu muno otumikira Yehova, koma otumikira Baala okha. 24Nalowa iwo kupereka nsembe zophera ndi nsembe zopsereza. Koma Yehu adadziikira kubwalo amuna makumi asanu ndi atatu, nati, Munthu akalola wina wa anthuwa ndirikuwaika m'manja mwanu apulumuke, moyo wace kulipa moyo wace. 25Ndipo kunali, atatsiriza kupereka nsembe yopsereza, Yehu anati kwa otumikira ndi atsogoleri, Lowani, akantheni; asaturuke ndi mmodzi yense. Nawakantha ndi lupanga lakuthwa; ndi otumikira ndi atsogoleri anawataya kubwalo, namuka ku mudzi wa nyumba ya Baala. 26Naturutsa zoimiritsa zija zinali m'nyumba ya Baala, nazitentha. 27Nagamula fane la Baala, nagamula nyumba ya Baala, naiyesa dzala mpaka lero lino. 28Momwemo Yehu anaononga Baala m'Israyeli.

Yehu apembedza mafano

29Koma Yehu sanazileka zoipa za Yerobiamu mwana wa Nebati, zimene adacimwitsa nazo Israyeli, ndizo ana a ng'ombe agolidi okhala m'Beteli ndi m'Dani. 30Ndipo Yehova anati kwa Yehu, Popeza wacita bwino, pocita coongoka pamaso panga, ndi kucitira nyumba ya Ahabu monga mwa zonse zinali m'mtima mwanga, ana ako a ku mbadwo wacinai adzakhala pa mpando wacifumu wa Israyeli. 31Koma Yehu sanasamalira kuyenda m'cilamulo ca Yehova Mulungu wa Israyeli ndi mtima wace wonse; sanaleka zoipa za Yerobiamu, zimene anacimwitsa nazo Israyeli.

32Masiku ao Yehova anayamba kusadza Israyeli; ndipo Hazaeli
anawakantha m'malire onse a Israyeli, 33kuyambira ku Yordano
kum'mawa, dziko lonse la Gileadi, la Agadi, ndi la Arubeni, ndi
Amanase, kuyambira ku Aroeri, ndiwo kumtsinje Arinoni, ndilo
Gileadi ndi Basana. 34Ndipo macitidwe ena a Yehu, ndi zonse
anazicita, ndi mphamvu yace yonse, sizinalembedwa kodi m'buku
la macitidwe a mafwnu a Israyeli 35Nagona Yehu ndi makolo ace,
namuika m'Samariya. Ndi Yehoahazi mwana wace anakhala
mfumu m'malo mwace. 36Ndipo masiku ace akukhala Yehu mfumu
ya Israyeli m'Samariya ndiwo zaka makumi awiri mphambu zisanu
ndi zitatu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

A taliya aononga mbumba yacifumu ya Yuda; apulumuka Yoasi, aphedwa Ataliya

1Pamene Ataliya mace wa Ahaziya anaona kuti mwana wace wafa,
ananyamuka, naononga mbeu yonse yacifumu. 2Koma Yoseba
mwana wa mfumu Yoramu, mlongo wace wa Ahaziya, anatenga
Yoasi mwana wa Ahaziya, namuba pakati pa ana a mfumu akuti
aphedwe, iye ndi mlezi, nawaika m'cipinda cogonamo; nambisira
Ataliya, ndipo sanaphedwa. 3Nakhala naye wobisika m'nyumba ya
Yehova zaka zisanu ndi cimodzi; ndipo Ataliya anakhala mfumu ya
dziko.
4Koma caka cacisanu ndi ciwiri Yehoyada anaitanitsa atsogoleri a
mazana a opha anthu, ndi a otumikira, nabwera nao kwa iye ku
nyumba ya Yehova, napangana nao, nawalumbiritsa m'nyumba ya
Yehova, nawaonetsa mwana wa mfumu. 5Nawalamulira, kuti,
Cocita inu ndi ici: limodzi la magawo atatu la inu olowa pa Sabata
lizilindira nyumba ya mfumu, 6ndi lina lizikhala ku cipata ca Suri,
ndi lina ku cipata kumbuyo kwa otumikira; momwemo muzisunga
nyumba, ndi kuicinjiriza. 7Ndipo magawo awiri ainu, ndiwo onse
oturukira pa Sabata, azilindira nyumba ya Yehova kuzinga
mfumu. 8Ndipo muzizinga mfumu, yense zida zace m'manja
mwace, ndi iye wakulowa poima inupo aphedwe; ndipo muzikhala
inu ndi mfumu poturuka ndi polowa iye. 9Ndipo atsogoleri a
mazana anacita monga mwa zonse anawalamulira Yehoyada
wansembe, natenga yense anthu ace olowera pa Sabata, ndi
oturukira pa Sabata, nafika kwa Yehoyada wansembeyo. 10Ndipo
wansembeyo anapereka kwa atsogoleri a mazana mikondo ndi
zikopa, zinali za mfumu Davide, zosungika m'nyumba ya
Yehova. 11Ndipo otumikira anakhala ciriri yense ndi zida zace
m'manja mwace, kuyambira mbali ya kulamanja kufikira mbali ya
kulamanzere ya nyumbayo, ku guwa la nsembe, ndi kunyumba,
kuzinga mfumu. 12Atatero, anaturutsa mwana wa mfumu, namuika
korona, nampatsa buku la umboni, namlonga ufumu, namdzoza,
naomba m'manja, nati, Mfomu ikhale ndi movo. 13Pamene Ataliya
anamva phokoso la otumikira ndi anthu, anadza kwa anthu
m'nyumba ya Yehova; 14napenya, ndipo taonani, mfumu iri ciriri
paciundo, monga adafocita, ndi atsogoleri ndi amalipenga pali
mfomu; nakondwerera anthu onse a m'dziko, naomba malipenga.
Pamenepo Ataliya anang'amba zobvala zace, napfuula, Ciwembu,
Ciwembu. 15Koma Yehoyada wansembe analamulira atsogoleri a
mazana oyang'anira khamu, nanena nao, Mumturutse mkaziyo
pabwalo pakati pa mipambo; womtsata iye mumuphe ndi lupanga;
pakuti wansembe adati, Asaphedwe m'nyumba ya Yehova. 16Ndipo

anamgwira, napita naye njira yolowera akavalo ku nyumba ya
mfumu, namupha pomwepo.
17Ndipo Yehoyada anacita cipangano pakati pa Yehova ndi mfomu
ndi anthu, akhale anthu a Yehova; pakati pa mfumunso ndi
anthu. 18Namuka anthu onse a m'dzikomo ku nyumba ya Baala,
naigumula; maguwa ace a nsembe ndi mafano ace anawaswaiswa,
napha Matana wansembe wa Baala ku maguwa a nsembe. Ndipo
wansembeyo anaika oyang'anira nyumba ya Yehova. 19Napita nao
atsogoleri a mazana, ndi opha anthu, ndi otumikira, ndi anthu onse
a m'dziko; ndipo iwo anatsika nayo mfumu ku nyumba ya Yehova,
nadzera njira ya cipata ca otumikira, kumka ku nyumba ya mfomu.
Nakhala Iye pa cimpando ca mafumu. 20Nakondwerera anthu onse
a m'dziko, ndi m'mudzi munali phe; ndipo adapha Ataliya ndi
lupanga ku nyumba ya mfumu. 21Yoasi anali wa zaka zisanu ndi
ziwiri polowa iye ufumu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Yoasi akonza Kacisi

1Caka cacisanu ndi ciwiri ca Yehu, Yoasi analowa ufumu wace;
nakhala mfumu m'Yerusalemu zaka makumi anai; ndi dzina la mai
wace ndiye Zibiya wa ku Beereseba. 2Ndipo Yoasi anacita
zoongoka pamaso pa Yehova masiku ace onse, m'mene
anamlangizira wansembe Yehoyada.
3Koma misanje sanaicotsa; anthu anapherabe nsembe, nafukiza
komisanje.
4Ndipo Yoasi anati kwa ansembe, Landirani ndarama zonse za
zinthu zopatulika azibwera nazo ku nyumba ya Yehova, ndizo
ndarama za otha msinkhu, ndarama za munthu ali yense monga
adamuyesa, ndi ndalama zimene yense azikumbuka m'mtima
mwace kuti abwere nazo ku nyumba ya Yehova. 5Ansembe
azilandire yense kwa iye amene adziwana naye, akonze nazo
mogamuka nyumba, pali ponse akapeza pogamuka. 6Koma kunali,
caka ca makumi awiri mphambu zitatu ca Yoasi sanathe kukonza
mogamuka nyumba. 7Pamenepo mfumu Yoasi anaitana Yehoyada
wansembe, ndi ansembe ena, nanena nao, Mulekeranji kukonza
mogamuka nyumba? Tsono musalandiranso ndarama kwa anzanu
odziwana nao, kuziperekera mogamuka nyumba. 8Nabvomera
ansembe kusalandiranso ndarama za anthu, kapena kukonza
mogamuka nvumba. 9Ndipo Yehoyada wansembe anatenga bokosi,
naboola ciboo pa cibvundikilo cace, naliika pafupi pa guwa la
nsembe, ku dzanja lamanja polowera nyumba ya Yehova; ndipo
ansembe akusunga pakhomo anaikamo ndarama zonse anabwera
nazo anthu ku nyumba ya Yehova, 10Ndipo pakuona kuti ndarama
zidacuruka m'bokosimo, anakwerako mlembi wa mfumu, ndi
mkuru wansembe, nazimanga m'matumba, naziyesa ndalama
zopereka m'nyumba ya Yehova. 11Napereka ndarama zoyesedwa
m'manja mwa iwo akucita nchitoyi, akuyang'anira nyumba ya
Yehova; ndipo iwo analipira nazo amisiri a mitengo ndi omanga,
akugwira nchito ya pa nyumba ya Yehova, 12ndi omanga miyala
ndi osema miyala, ndi kugula mitengo ndi miyala yosema
kukakonza mogamuka nyumba ya Yehova, ndi zonse zoigulira
nyumba zoikonzera. 13Koma sanapangira nyumba ya Yehova
mbale zasiliva, mbano, mbale zowazira, malipenga, zotengera ziri
zonse zagolidi, kapena zotengera ziri zonse zasiliva, kuzipanga ndi
ndarama adabwera nazo ku nyumba ya Yehova; 14pakuti
anazipereka kwa iwo akugwira nchitoyi, nakonza nazo nyumba ya
Yehova. 15Ndipo sanawerengera anthu, amene anapereka
ndaramazi m'manja mwao kuti apatse ogwira nchito; popeza
anacita mokhulupirika. 16Ndarama za nsembe zoparamula ndi

ndarama za nsembe yaucimo sanabwera nazo ku nyumba ya Yehova; nza ansembe izi.

Yoasi agonja kwa Hazaeli mfumu ya Aramu

17Pamenepo Hazaeli mfumu ya Aramu anakwera, nathira nkhondo pa Gati, naulanda, nalunjikitsa nkhope yace kukwera ku Yerusalemu. 18Koma Yoasi mfumu ya Yuda: anatenga zopatulika zonse adazipatula Yehosafati, ndi Yoramu, ndi Ahaziya, makolo ace, mafumu a Yuda, ndi zopatulika zace zace, ndi golidi yense anampeza pa cuma ca nyumba ya Yehova, ndi ca nyumba ya mfumu, nazitumiza kwa Hazaeli mfumu ya Aramu; motero anabwerera kucoka ku Yerusalemu. 19Macitidwe ena tsono a Yoasi ndi zonse adazicita sizilembedwa kodi m'buku la macitidwe a mafumu a Yuda? 20Ndipo anyamata ace ananyamuka, napangana, nakantha Yoasi ku nyumba ya Milo potsikira ku Silo. 21Pakuti Yozakara mwana wa Simeati, ndi Yosabadi mwana wa Someri, anyamata ace, anamkantha, nafa iye; ndipo anamuika kwa makolo ace m'mudzi wa Davide; ndi Amaziya mwana wace anakhala mfumu m'malo mwace.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Yoahazi mfumu ya Israyeli

1Caka ca makumi awiri ndi zitatu ca Yoasi mwana wa Ahaziya
mfumu ya Yuda, Yoahazimwana wa Yehu analowa ufumu wace wa
Israyeli ku Samariya, nakhala mfumu zaka khumi ndi zisanu ndi
ziwiri. 2Nacita coipa pamaso pa Yehova, natsata zolakwa za
Yerobiamu mwana wa Nebati, zimene analakwitsa nazo Israyeli;
sanazileka. 3Ndipo mkwiyo wa Yehova unayaka pa Israyeli,
nawapereka m'dzanja la Hazaeli mfumu ya Aramu, ndi m'dzanja la
Benihadadi mwana wa Hazaeli, masiku onsewoo 4Koma Yoahazi
anapembedza Yehova, Yehova namvera; pakuti anapenya
kupsinjika kwace kwa Israyeli m'mene mfumu ya Aramu
inawapsinja. 5Ndipo Yehova anapatsa Israyeli mpulumutsi,
naturuka iwo pansi pa dzanja la Aaramu; nakhala ana a Israyeli
m'mahema mwao monga kale. 6Komatu sanalekana nazo zolakwa
za nyumba ya Yerobiamu, zimene analakwitsa nazo Israyeli,
nayenda m'mwemo; nicitsalanso cifanizo m'Samariya. 7Koma
mfumu ya Aramu sanasiyira Yoahazi anthu, koma apakavalo
makumi asanu, ndi magareta khumi, ndi oyenda pansi zikwi khumi;
popeza mfumu ya Aramu anawaononga, nawayesa ngati pfumbi
lopondapo. 8Macitidwe ena tsono a Yoahazi, ndi zonse anazicita,
ndi mphamvu yace, sizilembedwa kodi m'buku la macitidwe a
mafumu a Israyeli? 9Ndipo Yoahazi anagona ndi makolo ace,
namuika m'Samariya; nakhala mfumu m'malo mwace Yoasi mwana
wace.

Yoasi mfumu ya Israyeli

10Caka ca makumi atatu ndi zisanu ndi ziwiri ca Yoasi mfumu ya
Yuda, Yoasi mwana wa Yoahazi analowa ufumu wace wa Israyeli
m'Samariya, nakhala mfumu zaka khumi ndi zisanu ndi
cimodzi. 11Nacita coipa pamaso pa Yehova, osazileka zolakwa
zonse za Yerobiamu mwana wa Nebati, zimene analakwitsa nazo
Israyeli, koma anayendamo. 12Macitidwe ena tsono a Yoasi, ndi
zonse anazicita, ndi mphamvu yace yocita nkhondo nayo pa
Amaziya mfumu ya Yuda, sizilembedwa kodi m'buku la macitidwe a
mafumu a Israyeli? 13Ndipo Yoasi anagona ndi makolo ace, ndi
Yerobiamu anakhala pa mpando wacifumu wace; namuika Yoasi
m'Samariya pamodzi ndi mafumu a Israyeli.

Kumwalira kwa Elisa

14Ndipo Elisa anadwala nthenda ija adafa nayo, namtsikira Yoasi
mfumu ya Israyeli, namlirira, nati, Atate wanga, atate wanga,
gareta wa Israyeli ndi apakavalo ace! 15Nanena naye Elisa, Tenga
uta ndi mibvi; nadzitengera uta ndi mibvi. 16Nati kwa mfumu ya
Israyeli, Pingiridzani. Napingiridza. Ndipo Elisa anasanjika manja
ace pa manja a mfumu. 17Nati, Tsegulani zenera la kum'mawa.

Nalitsegula. Nati Elisa, Ponyani. Naponya. Nati iye, Mubvi wa cipulumutso wa Yehova ndiwo mubvi wa kukupulumutsani kwa Aaramu; popeza mudzakantha Aaramu m'Afeki mpaka mudzawatha. 18Nati iye, Tengani mibvi; naitenga, Nati kwa mfumu ya Israyeli, Kwapula pansi; nakwapula katatu, naleka. 19Nakwiya naye munthu wa Mulungu, nati, Mukadakwapula kasanu, kapena kasanu ndi kamodzi; mukadatero, mukadadzakantha Aaramu mpaka kuwatha; koma tsopano mudzawakantha Aaramu katatu kokha.
20Pamenepo Elisa anamwalira, ndipo anamuika. Ndipo magulu a Amoabu analowa m'dziko poyambira caka. 21Ndipo anthu, pakuika maliro a munthu wina, anaona gulu la nkhondo, naponya mtembo m'manda mwa Elisa; koma pamene mtembowo unakhudza mafupa a Elisa, wakufayo anauka, naima ciriri.
22Ndipo Hazaeli mfumu ya Aramu anapsinja Israyeli masiku onse a Yoahazi. 23Koma Yehova analeza nao mtima, nawacitira cifundo, nawatembenukira; cifukwa ca cipangano cace ndi Abrahamu, Isake, ndi Yakobo, wosafuna kuwaononga, kapena kuwatayiratu pankhope pace. 24Nafa Hazaeli mfumu ya Aramu, nakhala mfumu m'malo mwace Benihadadi mwana wace. 25Ndi Yoasi mwana wa Yoahazi analandanso m'dzanja la Benihadadi mwana wa Hazaeli midzi ija adailanda m'dzanja la Yoahazi atate wace ndi nkhondo. Yoasi anamkantha katatu, naibweza midzi ya Israyeli.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Amaziyamfumu ya Yuda, Yoasi ndi Yerobiamu waciwiri mafumu a Israyeli

1Caka caciwiri ca Yoasi mwana wa Yoahazi mfumu ya Israyeli,
Amaziya mwana wa Yoasi mfumu ya Yuda analowa ufumu
wace. 2Ndiye wa zaka makumi awiri ndi zisanu polowa ufumu;
nakhala mfumu zaka makumi awiri mphambu zisanu ndi zinai
m'Yerusalemu; dzina la mace ndiye Yoadana wa ku
Yerusalemu. 3Ndipo anacita zoongoka pamaso pa Yehova, koma
wosanga Davide kholo lace; nacita monga mwa zonse anazicita
Yoasi atate wace. 4Koma misanje sanaicotsa; anthu anapherabe
nsembe, nafukiza pamisanje. 5Ndipo kunali, utakhazikika ufumu
m'dzanja lace, anakantha anyamata ace amene adakantha mfumu
atate wace; 6koma ana a ambandawo sanawapha, monga
mwalembedwa m'buku la cilamulo ca Mose, m'mene adalamulira
Yehova, ndi kuti, Atate asaphedwere ana, kapena ana kuphedwera
atate; koma yense afere kulak wa kwa iye yekha. 7Anapha Aedomu
m'Cigwa ca Mcere zikwi khumi, nalanda Sela ndi nkhondo, naucha
dzina lace Yokiteli mpaka lero lino.
8Pamenepo Amaziya anatuma mithenga kwa Yoasi mwana wa
Yoahazi mwana wa Yehu mfumu ya Israyeli, ndi kuti, Idzani tionane
maso. 9Natumiza Yoasi mfumu ya Israyeli kwa Amaziya mfumu ya
Yuda, ndi kuti, Mtungwi wa ku Lebano unatumiza mau kwa
mkungudza wa ku Lebano, ndi kuti, Mpatse mwana wanga
wamwamuna mwana wako wamkazi akhale mkazi wace; ndipo
Inapitapo nyama ya kuthengo ya ku Lebano, nipondereza
mtungwiwo. 10Wakanthadi Aedomu, koma mtima wako
wakukweza; ulemekezeke, nukhale kwanu; udziutsiranji tsoka,
ungagwe iwe ndi Yuda pamodzi nawe; 11Koma Amaziya
sanamvera. Motero anakwera Yoasi mfumu ya Israyeli, ndipo iye
ndi Amaziya mfumu ya Yuda anapenyana maso ku Betisemesi,
ndiwo wa Yuda. 12Nakanthidwa Yuda pamaso pa Israyeli, nathawira
yense kuhema kwace. 13Ndipo Yoasi mfumu ya Israyeli anagwira
Amaziya mfumu ya Yuda, mwana wa Yoasi mwana wa Ahaziya, ku
Betisemesi, nadza ku Yerusalemu, nagamula linga la Yerusalemu
kuyambira cipata ca Efraimu kufikira cipata ca kungondya, mikono
mazana anai. 14Natenga golidi ndi siliva yense, ndi zotengera
zonse anazipeza m'nyumba ya Yehova, ndi ku cuma ca m'nyumba
ya mfumu, acikole omwe; nabwera kumka ku
Samariya, 15Macitidwe ena tsono a Yoasi adazicita, ndi mphamvu
yace, ndi umo analimbana naye Amaziya mfumu ya Yuda,
sizilembedwa kodi m'buku la macitidwe a mafumu a
Israyeli? 16Nagona Yoasi ndi makolo ace, namuika m'Samariya

pamodzi ndi mafumu a Israyeli; nakhala mfumu m'malo mwace Yerobiamu mwana wace.
17Ndipo Amaziya mwana wa Yoasi mfumu ya Yuda anakhala ndi moyo, atamwalira Yoasi mwana wa Yoahazi mfumu ya Israyeli, zaka khumi ndi zisanu. 18Macitidwe ena tsono a Amaziya, kodi sizilembedwa m'buku la macitidwe a mafumu a Yuda? 19Ndipo anamcitira ciwembu m'Yerusalemu, nathawira iye ku Lakisi; koma anatumiza akumtsata ku Lakisi, namupha komweko. 20Nabwera naye pa akavalo, namuika ku Yerusalemu pamodzi ndi makolo ace m'mudzi wa Davide. 21Ndipo anthu onse a Yuda anatenga Azariya, (ndiye Uziya), ndiye wa zaka khumi mphambu zisanu ndi cimodzi, namlonga ufumu m'malo mwa atate wace Amaziya, 22Anamanga Elati, naubweza kwa Yuda, atagona ndi makolo ace mfumuyo.
23Caka cakhumi ndi zisanu ca Amaziya mwana wa Yoasi mfumu ya Yuda, Yerobiamu mwana wa Yoasi mfumu ya Israyeli analowa ufumu wace m'Samariya, nakhala mfumu zaka makumi anai mphambu cimodzi. 24Nacita iye coipa pamaso pa Yehova, sanaleka zolakwa zonse za Yerobiamu mwana wa Nebati, zimene analakwitsa nazo Israyeli. 25Anabweza malire a Israyeli kuyambira polowera ku Hamati mpaka nyanja ya kucidikha, monga mwa mau a Yehova Mulungu wa Israyeli, amene ananena ndi dzanja la mtumiki wace Yona mwana wa Amitai mneneriyo, ndiye wa Gati-heferi, 26Pakuti Yehova anapenya kuti kuzunzika kwao kwa Israyeli nkowawa ndithu; popeza panalibe womangika kapena womasuka, ndipo panalibe womthandiza Israyeli. 27Ndipo Yehova sadanena kuti adzafafaniza dzina la Israyeli pansi pa thambo; koma anawapulumutsa ndi dzanja la Yerobiamu mwana wa Yoasi. 28Macitidwe ena tsono a Yerobiamu, ndi zonse anazicita, ndi mphamvu yace, umo anacita nkhondo, nabweza kwa Israyeli Damasiko ndi Hamati amene anali a Yuda, sizilembedwa kodi m'buku la macitidwe a mafumu a Israyeli? 29Ndipo Yerobiamu anagona ndi makolo ace, ndiwo mafumu a Israyeli; nakhala mfumu m'malo mwace Zekariya mwana wace.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Azariya mfumu ya Yuda

1Caka ca makumi awiri mphambu zisanu ndi ziwiri ca Yerobiamu
mfumu ya Israyeli, Azariya mwana wa Amaziya mfumu ya Yuda
analowa ufumu wace. 2Anali wa zaka khumi ndi zisanu ndi cimodzi
polowa ufumu wace, nakhala mfumu zaka makumi asanu
mphambu ziwiri m'Yerusalemu; ndi dzina la mace ndiye Yekoliya
wa ku Yerusalemu. 3Nacita iye zoongoka pamaso pa Yehova,
monga mwa zonse adazicita atate wace Amaziya. 4Komatu
sanaicotsa misanje; anthu anapherabe nsembe, nafukiza
pamisanje. 5Ndipo Yehova anadwaza mfumu, nakhala iye wakhate
mpaka tsiku la imfa yace, nakhala m'nyumba ya padera. Ndipo
Yotamu mwana wa mfumu anayang'anira banja la mfumu,
naweruza anthu a m'dziko. 6Macitidwe ena tsono a Azariya, ndi
zonse anazicita, sizilembedwa kodi m'buku la macitidwe a mafumu
a Yuda? 7Nagona Azariya ndi makolo ace, namuika ndi makolo ace
m'mudzi wa Davide; nakhala mfumu m'malo mwace Yotamu
mwana wace.

Zekariya, Salumu, Menahemu, Pekahiya, Peka, mafumu a Israyeli

8Caka ca makumi atatu mphambu zisanu ndi zitatu ca Azariya
mfumu ya Yuda, Zekariya mwana wa Yerobiamu anakhala mfumu
ya Israyeli m'Samariya miyezi isanu ndi umodzi. 9Nacita iye coipa
pamaso pa Yehova, monga adacita makolo ace; sanaleka zolakwa
zace za Yerobiamu mwana wa Nebati, zimene analakwitsa nazo
Israyeli. 10Ndipo Salumu mwana wa Yabesi anamcitira ciwembu,
namkantha pamaso pa anthu, namupha; nakhala mfumu m'malo
mwace. 11Macitidwe ena tsono a Zekariya, taonani, zalembedwa
m'buku la macitidwe a mafumu a Israyeli. 12Awa ndi mau a Yehova
anawanena ndi Yehu, ndi kuti, Ana ako kufikira mbadwo wacinai
adzakhala pa mpando wacifumu wa Israyeli. Ndipo kunatero
momwemo.
13Salumu mwana wa Yabesi analowa ufumu wace caka ca makumi
atatu mphambu zisanu ndi zinai ca Uziya mfumu ya Yuda, nakhala
mfumu mwezi umodzi m'Samariya. 14Koma anakwera Menahemu
mwana wa Gadi kucokera ku Tiriza, nafika ku Samariya, nakantha
Salumu mwana wa Yabesi m'Samariya, namupha; nakhala mfumu
m'malo mwace. 15Macitidwe ena tsono a Salumu ndi ciwembu cace
anacicita, taonani, zalembedwa m'buku la macitidwe a mafumu a
Israyeli. 16Pamenepo Menahemu anakantha Tifisa, ndi onse anali
m'mwemo, ndi malire ace kuyambira ku Tiriza; popeza
sanamtsegulira pacipata; anaukantha, natumbula akazi onse a
pakati okhala m'mwemo.

17Caka ca makumi atatu mphambu zisanu ndi zinai ca Azariya
mfumu ya Yuda, Menahemu mwana wa Gadi analowa ufumu wace
wa Israyeti, nakhala mfumu zaka khumi m'Samariya. 18Nacita
coipa pamaso pa Yehova masiku ace onse, osaleka zolakwa za
Yerobiamu mwana wa Nebati, zimene analakwitsa nazo
Israyeli. 19Pamenepo Puli mfumu ya Asuri anadza kudzamenyana
ndi dziko, koma Menahemu anampatsa Puli matalente a siliva cikwi
cimodzi; kuti dzanja lace likhale naye kukhazikitsa ufumu m'dzanja
lace. 20Ndipo Menahemu anasonkhetsa Israyeli ndaramazi,
nasonkhetsa acuma, yense masekeli makumi asanu a siliva: kuti
azipereke kwa mfumu ya Asuri. Nabwerera mfumu ya Asuri
osakhala m'dzikomo. 21Macitidwe ena tsono a Menahemu, ndi
zonse anazicita, sizinalembedwa kodi m'buku la macitidwe a
mafumu a Israyeli? 22Nagona Menahemu ndi makolo ace; nakhala
mfumu m'malo mwace Pekahiya mwana wace.
23Caka ca makumi asanu a Azariya mfumu ya Yuda, Pekahiya
mwana wa Menahemu analowa ufumu wace wa Israyeli
m'Samariya, nakhala mfumu zaka ziwiri. 24Nacita coipa pamaso pa
Yehova, sanaleka zolakwa za Yerobiamu mwana wa Nebati, zimene
analakwitsa nazo Israyeli. 25Ndipo Peka mwana wa Remaliya,
kazembe wace, anamcitira ciwembu, nawakantha limodzi mfumu
ndi Arigobo ndi Ariye m'Samariya, m'nsanja ya ku nyumba ya
mfumu; pamodzi ndi iye panali amuna makumi asanu a Gileadi;
ndipo anamupha, nakhala mfumu m'malo mwace. 26Macitidwe ena
tsono a Pekahiya ndi zonse anazicita, taonani zalembedwa m'buku
la macitidwe a mafumu a Israyeli.
27Caka ca makumi asanu mphambu ziwiri ca Azariya mfumu ya
Yuda, Peka mwana wa Remaliya analowa ufumu wace wa Israyeli
m'Samariya, nakhala mfumu zaka makumi awiri. 28Nacita coipa
pamaso pa Yehova: osaleka zolakwa za Yerobiamu mwana wa
Nebati, zimene analakwitsa nazo Israyeli, 29Masiku a Peka mfumu
ya Israyeli anadza Tigilati Pilesere mfumu ya Asuri, nalanda Ijoni,
ndi Abeli-BeteMaaka, ndi Yanoa, ndi Kedesi, ndi Hazori, ndi Gileadi,
ndi Galileya, dziko lonse la Nafitali; nawatenga andende kumka
nao ku Asuri. 30Ndipo Hoseya mwana wa Ela anamcitira ciwembu
Peka mwana wa Remaliya, namkantha, namupha, nakhala mfumu
m'malo mwace caka ca makumi awiri ca Yotamu mwana wa
Uziya. 31Macitidwe ena tsono a Peka, ndi zonse anazicita, taonani,
zalembedwa m'buku la macitidwe a mafumu a Israyeli.

Yotamu mfumu ya Yuda

32Caka caciwiri ca Peka mwana wa Remaliya mfumu ya Israyeli,
Yotamu mwana wa Uziya mfumu ya Yuda analowa ufumu
wace. 33Ndiye wa zaka makumi awiri mphambu: zisanu polowa
ufumu wace, nakhalamfumu zaka khumi ndi zisanu ndi cimodzi

m'Yerusalemu; ndipo dzina la mace ndiye Yerusa mwana wa Zadoki. 34Nacita iye zoongoka pamaso pa Yehova; anacita monga mwa zonse anazicita atate; wace Uziya. 35Komatu sanaicotsa misanje; anthu anapherabe nsembe, nafukiza pamisanje. Iye anamanga cipata ca kumtunda ca nyumba ya Yehova. 36Macitidwe ena tsono a Yotamu, ndi zonse anazicita, sizilembedwa m'buku la macitidwe a mafumu a Yuda? 37Masiku awa Yehova anayamba kutumizira Yuda Rezini mfumu ya Aramu, ndi Peka mwana wa Remaliya, amenyane naye. 38Ndipo anagona Yotamu ndi makolo ace, namuika pamodzi ndi makolo ace m'mudzi wa Davide kholo lace; nakhala mfumu m'malo mwace Ahazi mwana wace.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Ahazi mfumu ya Yuda

1Caka cakhumi mphambu zisanu ndi ziwiri ca Peka mwana wa
Remaliya Ahazi mwana wa Yotamu mfumu ya Yuda analowa ufumu
wace. 2Ahazi anali wa zaka makumi awiri polowa ufumu wace,
nakhala mfumu zaka khumi mphambu zisanu ndi cimodzi
m'Yerusalemu; koma sanacita zoongoka pamaso pa Yehova
Mulungu wace, ngati Davide kholo lace; 3popeza anayenda m'njira
ya mafumu a Israyeli, napititsanso mwana wace pamoto, monga
mwa zonyansa za amitundu amene Yehova anawaingitsa pamaso
pa ana a Israyeli. 4Ndipo anaphera nsembe, nafukiza zonunkhira
kumisanje, ndi kuzitunda, ndi patsinde pa mtengo uli wonse
wogudira. 5Pamenepo Rezini mfumu ya Aramu, ndi Peka mwana
wa Remaliya mfumu ya Israyeli, anakwera kumka ku Yerusalemu
kukacita nkhondo, nammangira Ahazi misasa; koma sanakhoza
kumgonjetsa. 6Nthawi yomweyo Rezini mfumu ya Aramu
anabwezera Elati kwa Aramu, napitikitsa Ayuda ku Elati; nadza
Aaramu ku Elati, nakhala komweko kufikira lero lino. 7Ndipo Ahazi
anatuma mithenga kwa Tigilati Pilesere mfumu ya Asuri, ndi kuti,
Ine ndine kapolo wanu ndi mwana wanu; kwerani,
mudzandipulumutse m'dzanja la mfumu ya Aramu, ndi m'dzanja la
mfumu ya Israyeli anandiukirawo. 8Natenga Ahazi siliva ndi golidi
wopezeka m'nyumba ya Yehova, ndi ku cuma ca nyumba ya
mfumu, nazitumiza mtulo kwa mfumu ya Asuri. 9Nimmvera mfumu
ya Asuri, nikwera kumka ku Damasiko mfumu ya Asuri, niulanda,
nipita nao anthu ace andende ku Kiri, nimupha Rezini.

Guwa la nsembe la ku Damasiko

10Ndipo mfumu Ahazi anamuka ku Damasiko kukakomana ndi
Tigilati Pilesere mfumu ya Asuri, naona guwa la nsembe linali ku
Damasiko; natumiza mfumu Ahazi kwa Uriya wansembe
cithunzithunzi cace, ndi cifanizo cace, monga mwa mamangidwe
ace onse. 11Ndipo Uriya wansembe anamanga guwa la nsembelo,
monga mwa zonse anazitumiza mfumu Ahazi zocokera ku
Damasiko; momwemo Uriya wansembe analimanga asanabwere
mfumu ku Damasiko. 12Atafika mfumu kucokera ku Damasiko,
anapenya mfumu guwa la nsembelo, nayandikiza mfumu ku guwa
la nsembelo, napereka nsembe pomwepo. 13Nafukiza nsembe yace
yopsereza ndi nsemba yace yaufa, natsanulira nsembe yace
yothira, nawaza mwazi wa nsembe zace zamtendere pa guwa la
nsembelo, 14Nalicotsa guwa la nsembe lamkuwa linali pamasopa
Yehova, nalicotsa kukhomo la nyumba pakati pa guwa la nsembe
lace ndi nyumba ya Yehova, naliikakumpotokwa guwa la nsembe
lace. 15Ndipo mfumu Ahazi analamulira Uriya wansembe, kuti, Pa
guwa la nsembe lalikuru uzifukiza nsembe yopsereza yam'mawa,

ndi nsembe yaufa yamadzulo, ndi nsembe yopsereza ya mfumu, ndi nsembe yace yaufa, pamodzi ndi nsembe yopsereza ya anthu onse a m'dziko, ndi nsembe yao yaufa, ndi nsembe zao zothira; uziwaza pa ilo mwazi wonse wa nsembe yopsereza, ndi mwazi wonse wa nsembe yophera; koma guwa la nsembe lamkuwa ndi langa, lofunsira nalo. 16Nacita Uriya wansembe monga mwa zonse adalamulira mfumu Ahazi. 17Ndipo mfumu Ahazi anadula matsekerezo a maphaka, nacotsa mbiya pamwamba pao, natsitsa thawale pamwamba pa ng'ombe zamkuwa ziri pansi pace, naziika pa ciunda camiyala. 18Nacotsa ku nyumba ya Yehova malo ophimbika a pa Sabata adawamanga kunyumba, ndi polowera mfumu pofuma kunja, cifukwa ca mfumu ya Asuri. 19Macitidwe ena tsono adawacita Ahazi, salembedwa kodi m'buku la macitidwe a mafumu a Yuda? 20Nagona Ahazi ndi makolo ace, namuika ndi makolo ace m'mudzi wa Davide; nakhala mfumu m'malo mwace Hezekiya mwana wace.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Hoseyamfumu yotsiriza ya Israyeli, Salimanezeri mfumu ya Asuri apasula Samariya, Aisrayeli natengedwa ukapolo

1Caka cakhumi ndi ziwiri ca Ahazi mfumu ya Yuda Hoseya mwana
wa Ela analowa ufumu wace wa Israyeli m'Samariya, nakhala
mfumu zaka zisanu ndi zinai. 2Nacita iye coipa pamaso pa Yehova,
koma osati monga mafumu a Israyeli asanakhale
iye. 3Anamkwerera Salimanezere mfumu ya Asuri kumthira
nkhondo; ndipo Hoseya anamgonjera, namsonkhera mitulo. 4Koma
mfumu ya Asuri anampeza Hoseya alikucita ciwembu; popeza
anatuma mithenga kwa So mfumu ya ku Aigupto, osaperekanso
mtulo kwa mfumu ya Asuri, monga akacita caka ndi caka; cifukwa
cace mfumu ya Asuri anamtsekera, nammanga
m'kaidi. 5Pamenepo mfumu ya Asuri anakwera m'dziko monse,
nakwera ku Samariya, naumangira misasa zaka zitatu. 6Caka
cacisanu ndi cinai ca Hoseya mfumu ya Asuri analanda Samariya,
natenga Aisrayeli andende, kumka nao ku Asuri; nawakhalitsa
m'Hala, ndi m'Habori, ku mtsinje wa Gozani, ndi m'midzi ya
Amedi. 7Kudatero, popeza ana a Israyeli adacimwira Yehova
Mulungu wao, amene anawakweza kuwaturutsa m'dziko la Aigupto
pansi pa dzanja la Farao mfumu ya Aigupto, ndipo anaopa milungu
yina, 8nayenda m'miyambo ya amitundu amene Yehova
adawaingitsa pamaso pa ana a Israyeli, ndi m'miyambo ya
mafumu a Israyeli imene iwo anawalangiza. 9Ndipo ana a Israyeli
anacita m'tseri zinthu zosayenera pa Yehova Mulungu wao,
nadzimangira misanje m'midzi mwao monse ku nsanja ya olonda
ndi ku mudzi walinga komwe. 10Nadziimikira zoimiritsa ndi zifanizo
pa citunda ciri conse cacitali, ndi patsinde pa mtengo uli wonse
wogudira; 11nafukizapo zonunkhira pa misanje youse, monga umo
amacitira amitundu amene Yehova adawacotsa pamaso pao,
nacita zoipa kuutsa mkwiyo wa Yehova; 12natumikira mafano
amene Yehova anawanena nao, Musacita ici. 13Ndipo Yehova
anacitira umboni Israyeli ndi Yuda mwa dzanja la mneneri ali
yense, ndi mlauli ali yense, ndi kuti, Bwererani kuleka nchito zanu
zoipa, nimusunge malamulo anga ndi malemba anga, monga mwa
cilamulo conse ndinacilamulira makolo anu, ndi kucitumizira inu
mwa dzanja la atumiki anga aneneri. 14Koma sanamvera, naumitsa
khosi lao, monga khosi la makolo ao amene sanakhulupirira
Yehova Mulungu wao. 15Ndipo anakaniza malemba ace, ndi
cipangano anacicita ndi makolo ao, ndi mboni zace anawacitira
umboni nazo, natsata zopanda pace, nasanduka opanda pace,
natsata amitundu owazinga, amene Yehova adawalamulira nao,
kuti asacite monga iwowa. 16Ndipo anasiya malamulo onse a
Yehova Mulungu wao, nadzipangira mafano oyenga, ana a

ng'ombe awiri, napanga cifanizo, nagwadira khamu lonse la kuthambo, natumikira Baala. 17Napititsa ana ao amuna ndi akazi kumoto, naombeza ula, nacita zanyanga, nadzigulitsa kucita coipa pamaso pa Yehova, kuutsa mkwiyo wace. 18Cifukwa cace Yehova anakwiya naye Israyeli kwakukuru, nawacotsa pamaso pace osatsala mmodzi, koma pfuko la Yudalokha. 19Yudansosanasunga malamulo a Yehova Mulungu wao, koma anayenda m'malemba a Israyeli amene adawaika. 20Ndipo Yehova anakaniza mbumba yonse ya Israyeli, nawazunza, nawapereka m'dzanja la ofunkha, mpaka anawataya pamaso pace. 21Pakuti anang'amba Israyeli, kumcotsa ku nyumba ya Davide; ndipo anamlonga mfumu Yerobiamu mwana wa Nebati; Yerobiamu naingitsa Israyeli asatsate Yehova, nawalakwitsa kulakwa kwakukuru. 22Nayenda ana a Israyeli m'zolakwa zonse za Yerobiamu, zimene anazicita osazileka; 23mpaka Yehova adacotsa Israyeli pamaso pace, monga adanena mwa dzanja la atumiki ace onse aneneriwo. Momwemo Israyeli anacotsedwa m'dziko lao kumka nao ku Asuri mpaka lero lino.

Mfumu ya Asuri amangitsa alendo m'midzi ya Samariya

24Ndipo mfumu ya Asuri anabwera nao anthu ocokera ku Babulo, ndi ku Kuta, ndi ku Ava, ndi ku Hamati, ndi ku Safaravaimu, nawakhalitsa m'midzi ya Samariya, m'malo mwa ana a Israyeli; nakhala iwo eni ace a Samariya, nakhala m'midzi mwace. 25Ndipo kunali, poyamba iwo kukhala komweko, sanaopa Yehova; ndipo Yehova anawatumizira mikango, niwapha ena a iwowa. 26Motero ananena ndi mfumu ya Asuri, kuti, Amitundu aja mudawacotsa kwao, ndi kuwakhalitsa m'midzi ya Samariya, sadziwa makhalidwe a Mulungu wa dzikoli; cifukwa cace anawatumizira mikango pakati pao, ndipo taonani, irikuwapha; popeza sadziwa makhalidwe a Mulungu wa dzikoli. 27Pamenepo mfumu ya Asuri analamulira, kuti, Mukani naye komweko wina wa ansembe munawacotsako, nakakhale komweko, akawalangize makhalidwe a Mulungu wa dzikoli. 28Nadza wina wa ansembewo adawacotsa ku Samariya, nakhala ku Beteli, nawalangiza m'mene azimuopera Yehova. 29Koma a mtundu uli wonse anapanga milungu yao yao, naiika m'nyumba za misanje adazimanga Asamariya, a mtundu uli wonse m'midzi mwao mokhala iwo. 30Ndipo anthu a Babulo anapanga Sukoti Bemoti, ndi anthu a Kuta anapanga Nerigali, ndi anthu a Hamati anapanga Asima, 31ndi Aava anapanga Nibazi ndi Tarataka; ndi a Sefaravaimu anawatentha ana ao m'moto kwa Adrameleki, ndi Anameleki, milungu ya Asefaravaimu. 32Popeza anaopanso Yehova, anadziikira mwa iwo okha ansembe a misanje, ndiwo anaperekera nsembe m'nyumba za misanje. 33Amaopa Yehova, namatumikiranso milungu yao, monga mwa miyambo ya

amitundu anawacotsako. 34Mpaka lero lino acita monga mwa
miyambo yoyambayi; saopa Yehova, sacita monga mwa malemba
ao, kapena maweruzo ao, kapena cilamulo, kapena coikika
adacilamulira Yehova ana a Yakobo, amene anamucha
Israyeli, 35ndiwo amene Yehova adapangana nao, nawalamulira,
ndi kuti, Musamaopa milungu yina, kapena kuigwadira, kapena
kuitumikira, kapena kuiphera nsembe; 36koma Yehova amene
anakukwezani kukuturutsani m'dziko la Aigupto ndi mphamvu
yaikuru, ndi dzanja lotambasuka, Iyeyu muzimuopa, ndi Iyeyu
muzimgwadira, ndi Iyeyu muzimphera nsembe; 37ndi malemba,
ndimaweruzo, ndi cilamulo, ndi coikika anakulemberani
muzisamalira kuzicita masiku onse, nimusamaopa milungu:
yina; 38ndi cipangano ndinacicita nanu musamaciiwala, kapena
kuopa milungu yina iai; 39koma Yehova Mulungu wanu muzimuopa,
nadzakulanditsani Iyeyu m'dzanja la adani anu onse. 40Koma
sanamvera, nacita monga mwa mwambo wao woyamba. 41Ndipo
amitundu awa anaopa Yehova, natumikira mafano ao osema; ana
ao omwe, ndi zidzukulu zao zomwe, monga anacita makolo ao,
momwemo iwo omwe mpaka lero lino.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Hezekiya wabwino akhazikanso cipembedzo ca Yehova

1Ndipo kunali caka cacitatu ca Hoseya mwana wa Ela mfumu ya
Israyeli, Hezekiya mwana wa Ahazi mfumu ya Yuda analowa ufumu
waceo 2Ndiye wa zaka makumi awiri ndi zisanu polowa ufumu
wace, nakhala mfumu zaka makumi awiri mphambu zisanu ndi
zinai m'Yerusalemu; ndi dzina la mace ndiye Abi mwana wa
Zekariya. 3Nacita iye zoongoka pamaso pa Yehova, monga mwa
zonse adazicita Davide kholo lace. 4Anacotsa misanje, naphwanya
zoimiritsa, nalikha cifanizo, naphwanya njoka ija yamkuwa
adaipanga Mose; pakuti kufikira masiku awa ana a Israyeli
anaifukizira zonunkhira, naicha Cimkuwa. 5Anakhulupirira Yehova
Mulungu wa Israyeli; atafa iye panalibe wakunga iye mwa mafumu
onse a Yuda, ngakhale mwa iwo okhalapo asanabadwe iye. 6Pakuti
anaumirira Yehova osapambuka pambuyo pace, koma anasunga
malamulo amene Yehova adawalamulira Mose. 7Ndipo Yehova anali
naye, nacita iye mwanzeru kuli konse anamukako, napandukira
mfumu ya Asuri osamtumikira. 8Anakantha Afilisti mpaka Gaza ndi
malire ace, kuyambira nsanja ya olonda mpaka mudzi walinga.
9Ndipo kunali caka cacinai ca mfumu Hezekiya, ndico caka
cacisanu ndi ciwiri ca Hoseya mwana wa Ela mfumu ya Israyeli
Salimanezeri mfumu ya Asuri anakwerera Samariya, naumangira
misasa. 10Pakutha pace pa zaka zitatu anaulanda, ndico caka
cacisanu ndi cimodzi ca Hezekiya, ndico caka cacisanu ndi cinai ca
Hoseya mfumu ya Israyeli analanda Samariya. 11Ndipo mfumu ya
Asuri anacotsa Aisrayeli kumka nao ku Asuri, nawakhalitsa m'Hala,
ndi m'Habori, ku mtsinje wa Gozani, ndi m'midzi ya
Amedi; 12cifukwa sanamvera mau a Yehova Mulungu wao, koma
analakwira cipangano cace, ndico zonse anazilamulira Mose
mtumiki wa Yehova; sanazimvera kapena kuzicita.

Sanakeribu amangira Yerusalemu misasa

13Caka cakhumi ndi zinai ca Hezekiya Sanakeribu mfumu ya Asuri
anakwerera midzi yonse ya malinga ya Yuda, nailanda. 14Natumiza
Hezekiya mfumu ya Yuda kwa mfumu ya Asuri ku Lakisi, ndi kuti,
Ndalakwa; mundicokere; cimene mundisenzetse ndisenza.
Pamenepo mfumu ya Asuri anaikira Hezekiya mfumu ya Yuda
matalente mazana atatu a siliva ndi matalente makumi atatu a
golidi. 15Napereka Hezekiya siliva yense wopezeka m'nyumba ya
Yehova, ndi ku cuma ca nyumba yamfumu. 16Nthawi yomweyi
Hezekiya anakanganula golidi wa pa zitseko za Kacisi wa Yehova,
ndi pa zimphuthu adazikuta Hezekiya mfumu ya Yuda, nampereka
kwa mfumu ya Asuri. 17Ndipo mfumu ya Asuri anatuma nduna ndi
ndoda ndi kazembe ocokera ku Lakisi ndi khamu lalikuru la
nkhondo kwa mfumu Hezekiya ku Yerusalemu. Nakwera iwo, nafika

ku Yerusalemu. Ndipo atakwera, anafika, naima ku mcerenje wa thamanda la kumtunda, ndilo la ku mseu wa ku mwaniko wa otsuka nsaru. 18Ndipo m'mene adaitana mfumu, anawaturukira Eliyakimu mwana wa Hilikiya woyang'anira nyumba ya mfumu, ndi Sebina mlembi, ndi Yoa mwana wa Asafu wolemba mbiri. 19Nanena nao kazembeyo, Muuzetu Hezekiya, Itero mfumu yaikuru, mfumu ya Asuri, Cikhulupiriro ici ncotani ucikhulupirira? 20Ukuti koma ndiwo mau a pakamwa pokha, Pali uphungu ndi mphamvu ya kunkhondo. Tsono ukhulupirira yani, kuti undipandukira? 21Taona tsono ukhulupirira ndodo ya bango ili lothyoka, ndilo Aigupto; ndilo munthu akatsamirapo lidzamlowa m'dzanja lace ndi kulibola; atero Farao mfumu ya Aigupto kwa onse omkhulupirira iye. 22Ndipo mukati kwa ine, Tikhulupirira Yehova Mulungu wathu; sindiye amene Hezekiya wamcotsera misanje yace ndi maguwa a nsembe ace, nati kwa Yuda ndi kwa Yerusalemu, Muzilambira pa guwa la nsembe pane m'Yerusalemu? 23Mukokerane tsono ndi mbuye wanga mfumu ya Asuri, ndipo ndidzakupatsani akavalo zikwi ziwiri, mukakhoza inu kuonetsa apakavalo. 24Posakhoza kutero, mudzabweza bwanji nkhope ya nduna imodzi ya anyamata ang'ono a mbuye wanga, ndi kukhulupirira Aigupto akupatse magareta ndi apakavalo? 25Ngati ndakwerera malo ana wopanda Yehova, kuwaononga? Yehova anati kwa ine, Kwerera dziko ili ndi kuliononga. 26Pamenepo Eliyakimu mwana wa Hilikiya, ndi Sebina, ndi Yoa, anati kwa kazembeyo, Mulankhule ndi anyamata anu m'Ciaramu; popeza ticimva ici; musalankhule nafe m'Ciyuda, comveka ndi anthu okhala palinga. 27Koma kazembeyo ananena nao, Ngati mbuyanga ananditumiza kwa mbuyako, ndi kwa iwe, kunena mau awa? si kwa anthu awa nanga okhala palinga, kuti akadye zonyansa zao, ndi kumwa mkodzo wao pamodzi ndi inu? 28Naima kazembeyo, napfuula ndi mau akulu m'Ciyuda, nanena kuti, Tamverani mau a mfumu yaikuru mfumu ya Asuri. 29Itero mfumu, Asakunyengeni Hezekiya; pakuti sadzakhoza kukulanditsani m'dzanja lace; 30kapena Hezekiya asakukhulupiritseni pa Yehova, ndi kuti, Yehova adzatilanditsa ndithu, ndi mudzi uwu sudzaperekedwa m'dzanja la mfumu ya Asuri. 31Musamvere Hezekiya; pakuti Itero mfumu ya Asuri, Mupangane nane zamtendere, nimuturukire kwa ine, ndi kumadya yense ku mpesa wace, ndi yense ku mkuyu wace, ndi kumwa yense madzi a m'citsime cace; 32mpaka ndifika ndi kumuka nanu ku dziko lakunga dziko lanu, dziko la tirigu ndi vinyo, dziko la mkate ndi minda yampesa, dziko la azitona ndi la uci; kuti mukhale ndi moyo osafai; nimusamvere Hezekiya akakukopani, ndi kuti, Yehova adzatilanditsa. 33Kodi mlungu uli wonse wa amitundu walanditsa dziko lace m'dzanja la mfumu ya Asuri ndi kale

lonse? 34Iri kuti milungu ya Hamati, ndi ya Aripadi? iri kuti milungu
ya Sefaravaimu, kapena Hena, ndi Iva? Kodi yalanditsa Samariya
m'dzanja langa? 35Ndi yiti mwa milungu yonse ya maiko
inalanditsa maiko ao m'dzanja langa, kuti Yehova adzalanditsa
Yerusalemu m'dzanja langa? 36Koma anthuwo anakhala cete
osamyankha mau; pakuti lamulo la mfumu ndilo kuti,
Musamuyankha. 37Pamenepo Eliyakimu mwana wa Hilikiya
woyang'anira nyumba, ndi Sebina mlembi, ndi Yoa mwana wa
Asafu wolembera mbiri, anadza kwa Hezekiya ndi zobvala zao
zong'ambika, namuuza mau a kazembeyo.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Nkhawa ya Hezekiya ndi pemphero lace

1Ndipo kunali, atamva Hezekiya, anang'amba zobvala zace, napfundira ciguduli, nalowa m'nyumba ya Yehova. 2Natuma Eliyakimu woyang'anira nyumbayo, ndi Sebina mlembi, ndi akuru a ansembe opfundira ciguduli, kwa Yesaya mneneri mwana wa Amozi. 3Nati kwa iye, Atero Hezekiya, Lero line ndilo tsiku la cisautso, ndi la kudzudzula, ndi la kunyoza; pakuti ana anafikira kubadwa, koma palibe mphamvu yakubala. 4Kapena Yehova Mulungu wanu adzamva mau onse a kazembeyo, amene anamtuma mfumu ya Asuri mbuye wace, kuti atonze Mulungu wamoyo, nadzamlanga cifukwa ca mau adawamva Yehova Mulungu wanu; cifukwa cace uwakwezere otsalawo pemphero. 5Ndipo anyamata a mfumu Hezekiya anafika kwa Yesaya. 6Nanena nao Yesaya, Muzitero kwa mbuye wanu, Atero Yehova, Musamaopa mau mudawamva, amene anyamata a mfumu ya Asuri anandicitira nao mwano. 7Taonani, ndidzalonga mwa iye mzimu wakuti adzamva mbiri, nadzabwerera kumka ku dziko lace, ndipo ndidzamgwetsa ndi lupanga m'dziko lace.
8Nabwerera kazembeyo, napeza mfumu ya Asuri alikuthira nkhondo pa Libina, popeza anamva kuti adacoka ku Lakisi. 9Ndipo anamva za Tirihaka mfumu ya Kusi, akuti, Taonani, waturuka kuthirana nawe nkhondo. Pamenepo anatumizanso mithenga kwa Hezekiya, ndi kuti, 10Muzitero naye Hezekiya mfumu ya Yuda, kuti, Asakunyenge Mulungu wako amene umkhulupirira, ndi kuti, Yerusalemu sudzaperekedwa m'dzanja la mfumu ya Asuri. 11Taona, udamva ico mafumu a Asuri anacitira maiko onse, ndi kuwaononga konse; ndipo uti upulumuke ndiwe kodi? 12Kodi milunguyaamitundu inawalanditsa amene makolo anga anawaononga, ndiwo Gozani, ndi Hara Rezefi, ndi ana a Edeni okhala m'Telasara? 13Iri kuti mfumu ya Hamati, ndi mfumu ya Aripadi, ndi mfumu ya mudzi wa Sefaravaimu, wa Hena, ndi Iva? 14Ndipo Hezekiya analandira kalatayo ku dzanja la mithenga, namwerenga, nakwera Hezekiya kumka ku nyumba ya Yehova, namfunyulula pamaso pa Yehova. 15Napemphera Hezekiya pamaso pa Yehova, nati, Yehova Mulungu wa Israyeli wakukhala pakati pa akerubi, Inu ndinu Mulungu mwini wace, Inu nokha, wa maufumu onse a dziko lapansi; munalenga kumwamba ndi dziko lapansi. 16Cherani khutu lanu, Yehova, nimumve; tsegulani maso anu, Yehova, nimupenye; ndipo imvani mau a Sanakeribu, amene anatumiza kutonza nao Mulungu wamoyo. 17Zoona, Yehova, mafumu a Asuri anapasula amitundu ndi maiko ao, 18naponya milungu yao kumoto; popeza sindiyo milungu koma yopanga anthu ndi manja ao, mtengo ndi mwala; cifukwa cace anaiononga. 19Ndipo tsono, Yehova Mulungu wathu, mutipulumutse m'dzanja lace, kuti adziwe maufumu onse a dziko lapansi kuti Inu ndinu Yehova Mulungu, Inu nokha nokha.

Yesaya amtonthoza mtima Hezekiya

20Pamenepo Yesaya mwana wa Amozi anatumiza kwa Hezekiya, ndi, kuti, Atero Yehova Mulungu wa Israyeli, Condipempha iwe pa Sanakeribu mfumu ya Asuri ndacimva. 21Mau a Yehova akumnenera iye ndi awa, Namwali mwana wamkazi wa Ziyoni akunyoza, akuseka mwana wamkazi wa Yerusalemu, akupukusira mutu pambuyo pako. 22Ndiye yani wamtonza ndi kumcitira mwano? ndiye yani wamkwezera mau ndi kumgadamira maso ako m'mwamba? Ndiye Woyerayo wa Israyeli. 23Watonza Yehova mwa mithenga yako, nuti, Ndi magareta anga aunyinji ndakwera pa misanje ya mapiri ku mbali zace za Lebano, ndipo ndidzagwetsa mikungudza yace yaitali, ndi mitengo yace yosankhika yar mlombwa, ndidzalowanso m'ngaka mwace mweni mweni, ku nkhalango zace za madimba. 24Ndakapa, ndamwa madzi

acilendo, ndi ku mapazi anga ndidzaphwetsa mitsinje yonse ya
Aigupto, 25Sunamva kodi kuti Ine ndinacicita kale lomwe, ndi kucipanga
masiku akalekale? tsopano ndacifikitsa kuli iwe, uzikhala wakupasula imidzi
yamalinga ikhale miunda ya mabwinja. 26Cifukwa cace okhalamo ao anali
ofok a manja, anaopsedwa, nacita manyazi, ananga udzu wa kuthengo, ndi
msipu wauwisi, ndi udzu wa patsindwi, ndi tirigu wopserera
asanakule. 27Koma ndidziwa kukhala pansi kwako, ndi kuturuka kwako, ndi
kulowa kwako, ndi kundizazira kwako. 28Cifukwa ca kundizazira kwako, ndi
popeza kudzikuza kwako kwandifikira m'makutu mwanga, ndidzakukowa ndi
ngowe yanga m'mphuno mwako, ndi cam'kamwa canga m'milomo mwako;
ndipo ndidzakubwezera pa njira unadzerayi. 29Ndi ici ndi cizindikilo cako: caka
cino mudzadya za mphulumukwa, ndi caka ca mawa za mankhokwe, ndi caka
camkuca muzibzala ndi kukolola, muzioka minda yampesa ndi kudya zipatso
zace. 30Ndipo opulumuka a nyumba ya Yuda otsalawo adzaphukanso mizu,
ndi kupatsa zipatso pamwamba. 31Pakuti ku Yerusalemu kudzaturuka otsala,
ndi akupulumukawo ku phiri la Ziyoni; cangu ca Yehova cidzacita
ici. 32Cifukwa cace atero Yehova za mfumu ya Asuri, iye sadzalowa m'mudzi
muno, kapena kuponyamo mubvi, kapena kufikako ndi cikopa, kapena
kuundira mtumbira. 33Adzabwerera njira yomweyo anadzera, ndipo sadzalowa
m'mudzi muno, ati Yehova. 34Pakuti ndidzacinjiriza mudzi uno kuupulumutsa,
cifukwa ca Ine mwini, ndi cifukwa ca Davide mtumiki wanga.

Mthenga wa Yehova awapha Aasurio

35Ndipo kunali, usiku womwewo mthenga wa Yehova anaturuka, nakantha
m'misasa ya Aasuri zikwi zana limodzi mphambu makumi asanu ndi atatu
kudza zisanu, ndipo pouka anthu mamawa, taonani, onsewo ndi
mitembo. 36Nacoka Sanakeribu mfumu ya Asuri, namuka, nabwerera, nakhala
ku Nineve. 37Ndipokunali popembedza iye m'nyumba ya Nisiroki mulungu
wace, Adrameleki ndi Sarezere anamkantha ndi lupanga; napulumukira ku
dziko la Ararati. Ndipo Esarihadoni mwana wace anakhala mfumu m'malo
mwace.

Hezekiya adwala nacira

1Masiku ajawo Hezekiya anadwala, nafuna kufa. Namdzera Yesaya mneneri
mwana wa Amozi, nanena naye, Atero Yehova, Siyira banja lako; pakuti
udzafa, sudzakhala ndi moyo. 2Pamenepo anatembenuzira nkhope yace
kukhoma, napemphera kwa Yehova, ndi kuti, 3Mukumbukile Yehova kuti
ndinayendabe pamaso panu m'coonadi, ndi mtima wangwiro, ndi kucita
zokoma m'kuona kwanu. Nalira Hezekiya kulira kwakukuru. 4Ndipo kunali,
asanaturukire Yesaya m'kati mwa mudzi, anamdzera mau a Yehova, ndi
kuti, 5Bwerera, nunene kwa Hezekiya mtsogoleri wa anthu anga, Atero Yehova
Mulungu wa Davide kholo lako, Ndamva pemphero lako, ndapenya misozi
yako; taona, nelidzakuciritsa, tsiku lacitatu udzakwera kumka ku nyumba ya
Yehova. 6Ndipo ndakuonjezera pa masiku ako zaka khumi ndi zisanu;
ndidzakupulumutsa iwe ndi mudzi uno m'dzanja la mfumu ya Asuri;
ndidzacinjiriza mudzi uno, cifukwa ca Ine ndekha, ndi cifukwa ca Davide
mtumiki wanga. 7Nati Yesaya, Tenga ncinci yankhuyu. Naitenga, naiika
papfundo, nacira iye. 8Nati Hezekiya kwa Yesaya, Cizindikilo cace nciani kuti
Yehova adzandiciza, ndi kuti ndidzakwera kumka ku nyumba ya Yehova tsiku
lacitatu? 9Nati Yesaya, Cizindikilo ndici akupatsa Yehova, kuti Yehova
adzacicita conena iye; kodi mthunzi umuke m'tsogolo makwerero khumi,
kapena ubwerere m'mbuyo makwerero khumi? 10Nati Hezekiya, Kutsikira
mthunzi makwerero khumi nkopepuka, kutero ai; koma mthunzi ubwerere
makwerero khumi. 11Napfuulirakwa Yehova Yesayamneneriyo, nabweza iye
mthunzi m'mbuyo makwerero khumi, ndiwo amene udatsikira pa makwerero a
Ahazi.

Hezekiya acimwa mwa kuonetsa cuma cace

12Nthawi ija Berodaki Baladani mwana wa Baladani mfumu ya Sabulo
anatumiza akalata ndi mtulo kwa Hezekiya, popeza adamva kuti adadwala
Hezekiya. 13Ndipo Hezekiya anawamvera, nawaonetsa nyumba yonse ya
cuma cace, siliva, ndi golidi, ndi zonunkhira, ndi mafuta okometsetsa, ndi
nyumba ya zida zace, ndi zonse zopezeka pacuma pace; panalibe kanthu
m'nyumba mwace, kapena m'ufumu wace wonse osawaonetsa
Hezekiya. 14Koma Yesaya mneneri anadza kwa mfumu Hezekiya, nati kwa iye,
Anatani anthu awa? anadza kwa inu kufumira kuti? Nati Hezekiya, Afumira
dziko la kutari ku Babulo. 15Nati iye, Anaona ciani m'nyumba mwanu? Nati
Hezekiya, Zonse za m'nyumba mwanga anaziona, palibe kanthu pacuma
canga kosawaonetsa. 16Ndipo Yesaya anati kwa Hezekiya, Tamverani mau a
Yehova. 17Taonani, akudza masiku kuti zonse za m'nyumba mwako, ndi
zokundika makolo ako mpaka lero, zidzatengedwa kumka ku Babulo,
kosasiyidwa kanthu konse, ati Yehova. 18Nadzatenga ena a ana ako oturuka
mwa iwe, amene udzawabala, nadzakhala iwo adindo m'cinyumba ca mfumu
ya Babulo. 19Pamenepo Hezekiya anati kwa Yesaya, Mau a Yehova udawanena
ndi abwino. Natinso, Si momwemo nanga, mtendere ndi coonaeli zikakhala
masiku anga? 20Macitidwe ena tsono a Hezekiya, ndi mphamvu yace yonse,
ndi umo anamangira dziwe ndi mcera, nautengera mudzi madzi, sizilembedwa
kodi m'buku la macitidwe a mafumu a Yuda? 21Nagona Hezekiya ndi makolo
ace; nakhala mfumu m'malo mwace Manase mwana wace.

Manase woipitsitsa

1Manase anali wa zaka khumi ndi ziwiri polowa iye ufumu wace,
nakhala mfumu zaka makumi asanu ndi zisanu m'Yerusalemu; ndi
dzina la mace ndiye Hefisiba. 2Ndipo anacita coipa pamaso pa
Yehova, monga mwa zonyansa za amitundu amene Yehova
anawaingitsa pamaso pa ana a Israyeli. 3Pakuti anamanganso
misanje, imene Hezekiya atate wace adaiononga; nautsira Baala
maguwa a nsembe, nasema cifanizo, monga anacita Ahabu mfumu
ya Israyeli, nagwadira khamu lonse la kuthambo,
nalitumikira. 4Namanga iye maguwa a nsembe m'nyumba ya
Yehova imene Yehova adainenera kuti, M'Yerusalemu ndidzaika
dzina langa. 5Nalimangira khamu lonse la kuthambo maguwa a
nsembe m'mabwalo awiri a nyumba ya Yehova. 6Napititsa mwana
wace pamoto, naombeza maula, nacita zanyanga, naika
obwebweta ndi openda; anacita zoipa zambiri pamaso pa Yehova
kuutsa mkwiyo wace. 7Ndipo anaika cifanizo cosema cimene
adacipanga m'nyumba ija Yehova adainenera kwa Davide ndi kwa
Solomo mwana wace kuti, M'nyumba muno ndi m'Yerusalemu
umene ndausankha mwa mafuko onse a Israyeli ndidzaikamo
dzina langa kosatha. 8Ndipo sindidzacotsanso mapazi a Israyeli
m'dziko ndidalipereka kwa makolo ao; cokhaci asamalire kucita
monga mwa zonse ndawalamulira ndi monga mwa cilamulo conse
anawalamulira Mose mtumiki wanga. 9Koma sanamvera,
nawalakwitsa Manase, nawacititsa coipa, kuposa amitundu amene
Yehova adawaononga pamaso pa ana a Israyeli. 10Pamenepo
Yehova ananena mwa atumiki ace aneneri, ndi kuti, 11Popeza
Manase mfumu ya Yuda anacita zonyansa izi, pakuti zoipa zace
zinaposa zonse adazicita Aamori, amene analipo asanabadwe iye,
nalakwitsanso Yuda ndi mafano ace; 12cifukwa cace atero Yehova
Mulungu wa Israyeli, Taonani, nditengera Yerusalemu ndi Yuda
coipa, cakuti yense acimvera cidzamliritsa mwini khutu. 13Ndipo
ndidzayesa pa Yerusalemu cingwe coongolera ca Samariya, ndi
cingwe colungamitsira ciriri ca nyumba ya Ahabu; ndidzapukuta
Yerusalemu monga umo apukutira mbale, kuipukuta ndi
kuibvundikira. 14Ndipo ndidzataya cotsala ca colowa canga, ndi
kuwapereka m'dzanja la adani ao, nadzakhala iwo cakudya ndi
cofunkha ca adani ao onse; 15popeza anacita coipa pamaso panga,
nautsa mkwiyo wanga citurukire makolo ao m'Aigupto, mpaka lero
lino. 16Ndiponso Manase anakhetsa mwazi wambiri wosacimwa
mpaka anadzaza m'Yerusalemu monsemo, osawerenga kulakwa
kwace analakwitsa nako Yuda, ndi kucita coipa pamaso pa
Yehova. 17Macitidwe ena tsono a Manase, ndi zonse anazicita,
sizilembedwa kodi m'buku la macitidwe a mafumu a

Yuda? 18Nagona Manase ndi makolo ace, naikidwa m'munda wa
nyumba yace, m'munda wa Uza, nakhala mfumu m'malo mwace
Amoni mwana wace.

Amoni mfumu ya Yuda

19Amoni anali wa zaka makumi awiri mphambu ziwiri polowa iye
ufumu wace, nakhala mfumu zaka ziwiri m'Yerusalemu; ndi dzina
la mace ndiye Mesulemeti mwana wa Haruzi wa ku Yotiba. 20Nacita
iye coipa pamaso pa Yehova, monga umo amacitira Manase atate
wace. 21Nayenda iye m'njira monse anayendamo atate wace,
natumikira mafano anawatumikira atate wace,
nawagwadira; 22nasiya Yehova Mulungu wa makolo ace,
sanayenda m'njira ya Yehova. 23Ndipo anyamata ace a Amoni
anamcitira ciwembu, napha mfumuyo m'nyumba yace
yace. 24Koma anthu a m'dzikomo anapha onse akumcitira ciwembu
mfumu Amoni; ndipo anthu a m'dzikomo anamlonga ufumu Yosiya
mwana wace m'malo mwace. 25Macitidwe ena tsono a Amoni
adawacita, salembedwa kodi m'buku la macitidwe a mafumu a
Yuda? 26Naikidwa iye m'manda mwace m'munda wa Uza;
nakhalamfumum'malo mwace Yosiya mwana wace.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Yosiya wabwino akonzanso kacisi

1Yosiya ndiye wa zaka zisanu ndi zitatu polowa ufumu wace,
nakhala mfumu zaka makumi atatu mphambu cimodzi
m'Yerusalemu; ndi dzina la mace ndi Yedida mwana wa Adaya wa
ku Bozikati. 2Nacita iye zoongoka pamaso pa Yehova, nayenda
m'njira yonse ya Davide kholo lace, osapambukira ku dzanja
lamanja kapena kulamanzere.
3Ndipo kunali caka cakhumi mphambu zisanu ndi zitatu ca Yosiya,
mfumuyi inatuma Safani mwana wa Azaliya mwana wa Mesulamu,
mlembi, ku nyumba ya Yehova, ndi kuti, 4Kwera kwa Hilikiya mkulu
wa ansembe, awerenge ndalama zimene anthu anabwera nazo ku
nyumba ya Yehova, ndizo zimene olindira pakhomo anasonkhetsa
anthu; azipereke m'dzanja anchito akuyang'anira nyumba ya
Yehova; 5iwo azipereke kwa ogwira nchito ya m'nyumba ya Yehova,
akonze mogamuka nyumbayi, 6kwa amisiri a mitengo, ndi omanga
nyumba, ndi omanga linga; ndi kuti agule mitengo ndi miyala
yosema kukonza nazo nyumbayi. 7Koma sanawawerengera
ndalamazo zoperekedwa m'dzanja lao, pakuti anacita
mokhulupirika.

Hilikiya apeza buku la cilamulo

8Ndipo Hilikiya mkulu wa ansembe anati kwa Safani mlembi,
Ndapeza buku la cilamulo m'nyumba ya Yehova. Napereka Hilikiya
bukulo kwa Safani, iye naliwerenga. 9Ndipo Safani mlembiyo
anadza kwa mfumu, nambwezera mfumu mau, nati, Anyamata anu
anakhuthula ndalama zopereka m'nyumba, nazipereka m'dzanja la
anchito akuyang'anira nyumba ya Yehova. 10Ndipo Safani
mlembiyo anafotokozera mfumu, ndi kuti, Hilikiya wansembe
wandipatsa buku. Nawerengamo Safani pamaso pa
mfumu. 11Ndipo kunali, atamva mfumu mau a m'buku la cilamulo,
inang'amba zobvala zace. 12Ndipo mfumu inalamulira Hilikiya
wansembe, ndi Ahikamu mwana wa Safani, ndi Alabori mwana wa
Mikaya, ndi Safani mlembi, ndi Asaya mnyamata wa mfumu, ndi
kuti, 13Mukani, funsirani ine, ndi anthu, ndi Yuda yense, kwa
Yehova za mau a buku ili adalipeza; pakuti mkwiyo wa Yehova
wotiyakira ife ndi waukuru; popeza atate athu sanamvera mau a
buku ili, kucita monga mwa zonse zotilemberamo.

Hulida mneneri wamkazi

14Namuka Hilikiya wansembe, ndi Ahikamu, ndi Akibori, ndi Safani,
ndi Asaya, kwa Hulida mneneri wamkazi, ndiye mkazi wa Salumu
mwana wa Tlkiva, mwana wa Harasi, wosunga zobvala za mfumu;
analikukhala iye m'Yerusalemu m'dera laciwiri, nalankhula
naye. 15Ndipo Hulida ananena nao, Atero Yehova Mulungu wa
Israyeli, Muuze munthuyo anakutumizani kwa ine, 16Atero Yehova,

Ta, onani, nditengera maloano coipa, ndi iwo okhalamo,
cokwaniritsa mau onse a m'buku adaliwerenga mfumu ya
Yuda; 17popeza anandisiya Ine, nafukizira zonunkhira milungu yina,
kuti autse mkwiyo wanga ndi nchito zonse za manja ao; cifukwa
cace mkwiyo wanga udzayakira malo ana wosazimikanso. 18Koma
kwa mfumu ya Yuda amene anakutumizani kufunsira kwa Yehova,
muzitero naye, Atero Yehova Mulungu wa Israyeli, Kunena za mau
udawamva, 19popeza mtima wako ngoolowa, ndipo unadzicepetsa
pamaso pa Yehova muja udamva zonenera Ine malo ana ndi anthu
okhalamo, kuti adzakhala abwinja, ndi temberero; ndipo
unang'amba zobvala zako ndi kulira misozi pamaso panga, Inenso
ndakumvera, ati Yehova. 20Cifukwa cace, taona,
ndidzakusonkhanitsa ukhale ndi makolo ako, nudzatengedwa
ulowe m'manda mwako mumtendere; ndipo sudzaona m'maso
mwako coipa conse ndidzacifikitsira malo ano. Ndipo anambwezera
mfumu mau.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Yosiya awerenga bukulo kwa anthu nacita pangano ndi Yehova, nakonza zoipsa zambiri

1Pamenepo mfumu inatumiza anthu, namsonkhanitsira akulu onse
a Yuda ndi a m'Yerusalemu. 2Nikwera mfumu kumka ku nyumba ya
Yehova, ndi amuna onse a Yuda, ndi onse okhala m'Yerusalemu
pamodzi nave, ndi ansembe, ndi aneneri, ndi anthu onse ang'ono
ndi akulu; nawerenga iye m'makutu mwao mau onse a m'buku la
cipangano adalipeza m'nyumba ya Yehova. 3Niima mfumu
paciunda, nicita pangano pamaso pa Yehova, kutsata Yehova, ndi
kusunga malamulo ace, ndi mboni zace, ndi malemba ace, ndi
mtima wonse ndi moyo wonse, kukhazikitsa mau a cipangano
colembedwa m'buku ili; ndipo anthu onse anaimiririra
panganoli. 4Ndipo mfumu inalamulira Hilikiya mkulu wa ansembe,
ndi ansembe a gawo laciwiri, ndi olindira pakhomo, aturutse
m'Kacisi wa Yehova zipangizo adazipangira Baala, ndi cifanizo cija,
ndi khamu lonse la kuthambo; nazitentha kunja kwa Yerusalemu ku
thengo la ku Kidroni, natenga phulusa lace kumka nalo ku
Beteli. 5Naletsa ansembe opembedza mafano, amene mafumu a
Yuda anawaika afukize zonunkhira pa misanje m'midzi ya Yuda, ndi
pamalo pozinga Yerusalemu; wo omwe ofukizira zonunkhira Baala,
ndi dzuwa, ndi mwezi, ndi nthanda, ndi khamu lonse la
kuthambo. 6Naturutsa cifanizoco m'nyumba ya Yehova kunja kwa
Yerusalemu ku mtsinje wa Kidroni; nacitenthera ku mtsinje wa
Kidroni, nacipera cikhale pfumbi, naliwaza pfumbi lace pa manda a
ana a anthu. 7Nagamula nyumba za anyamata adama okhala ku
nyumba ya Yehova, kumene akazi anaomba nsaru zolenjeka za
cifanizoco. 8Naturutsa ansembe onse m'midzi ya Yuda, nawaipitsira
misanje, imene ansembe adafukizapo zonunkhira, kuyambira Geba
kufikira Beereseba; napasula misanje ya kuzipata, yokhala
polowera pa cipata ca Yoswa kazembe wa mudzi, yokhala ku
dzanja lako lamanzere kwa cipata ca mudzi. 9Koma ansembe a
misanje sanakwera kudza ku guwa la nsembe la Yehova ku
Yerusalemu; koma anadya mkate wopanda cotupitsa pakati pa
abale ao. 10Anawaipitsiranso Tofeti, wokhala m'cigwa ca ana a
Hinomu; kuti asapitirize mmodzi yense mwana wace wamwamuna
kapena wamkazi pamoto kwa Moleki. 11Nacotsanso akavalo amene
mafumu a Yuda adapereka kwa dzuwa, polowera nyumba ya
Yehova, ku cipinda ca Natani Meleki mdindoyo, cokhala kukhonde;
natentha magareta a dzuwa ndi moto. 12Ndi maguwa a nsembe
anali patsindwi pa cipinda cosanja ca Ahazi adawapanga mafumu a
Yuda, ndi maguwa a nsembe adawapanga Manase m'mabwalo
awiri a nyumba ya Yehova, mfumu inawagumula, niwacotsa
komweko, nitaya pfumbi lao ku mtsinje wa Kidroni. 13Ndipo mfumu

inawaipitsira misanje yokhala kum'mawa kwa Yerusalemu, ndiyo
ya ku dzanja lamanja la phiri la cionongeko, imene Solomo mfumu
ya Israyeli adaimangira Asitoreti conyansa ca Asidoni, ndi Kemosi
conyansa ca Moabu, ndi Milikomu conyansa ca ana a
Amoni. 14Nathyolathyola zoimiritsa, nalikha zifanizo, nadzaza
pamalo pao ndi mafupa a anthu. 15Anagumulanso guwa la nsembe
linali ku Beteli, ndi msanje adaumanga Yerobiamu mwana wa
Nebati wolakwitsa Israyeli uja; guwa la nsembelo, ndi msanje
womwe anagumula; natentha msanje, naupondereza ukhale
pfumbi, natentha cifanizoco. 16Ndipo potembenuka Yosiya anaona
manda okhalako kuphiri, natumiza anthu naturutsa mafupa
kumanda, nawatentha pa guwa la nsembe, kuliipitsa, monga mwa
mau a Yehova anawalalikira munthu wa Mulungu wolalikira
izi. 17Anatinso, Cizindikilo ici ndiciona nciani? Namuuza anthu a
m'mudziwo, Ndico manda a munthu wa Mulungu anafuma ku Yuda,
nalalikira izi mwazicitira guwa la nsembe la ku Beteli. 18Nati iye,
Mlekeni, munthu asakhudze mafupa ace. Naleka iwo mafupa ace
akhale pamodzi ndi mafupa a mneneri uja anaturuka
m'Samariya. 19Ndi nyumba zonse zoo mwe za ku misanje yokhala
m'midzi ya Samariya, adazimanga mafumu a Israyeli kuutsa nazo
mkwiyo wa Yehova, Yosiya anazicotsa, nazicitira monga mwa
nchito zonse adazicita ku Beteli. 20Ndipo anapha ansembe onse a
misanje okhalako pa maguwa a nsembe, natentha-mafupa a anthu
pamenepo, nabwerera kumka ku Yerusalemu.

Acita Paskha

21Ndipo mfumu inalamulira anthu onse, kuti, Mcitireni Yehova
Mulungu wanu Paskha, monga mulembedwa m'buku ili la
cipangano, 22Zedi silinacitika Paskha lotere ciyambire masiku a
oweruza anaweruza Israyeli, ngakhale m'masiku a mafumu a
Israyeli, kapena mafumu a Yuda; 23koma Paskha ili analicitira
Yehova m'Yerusalemu, Yosiya atakhala mfumu zaka khumi
mphambu zisanu ndi zitatu. 24Ndiponso obwebweta, ndi openda,
ndi aterafi, ndi mafano, ndi zonyansa zonse zidaoneka m'dziko la
Yuda ndi m'Yerusalemu, Yosiya anazicotsa; kuti alimbitse mau a
cilamulo olembedwa m'buku adalipeza Hilikiya wansembe
m'nyumba ya Yehova. 25Ndipo asanabadwe iye panalibe mfumu
wolingana naye, imene inatembenukira kwa Yehova ndi mtima
wace wonse, ndi moyo wace wonse, ndi mphamvu yace yonse,
monga mwa cilamulo conse ca Mose; atafa iyeyu sanaukanso wina
wolingana naye. 26Koma Yehova sanakululuka mkwiyo wace
waukuru waukali umene adapsa mtima nao pa Yuda, cifukwa ca
zoputa zonse Manase adaputa nazo mkwiyo wace. 27Nati Yehova,
Ndidzacotsa Yudanso pamaso panga, monga umo ndinacotsera
Israyeli; ndipo ndidzataya mudzi uwu ndidausankha, ndiwo

Yerusalemu, ndi nyumba ndidainena, Dzina langa lidzakhala komweko. 28Macitidwe ena tsono a Yosiya, ndi zonse anazicita, sizilembedwa kodi m'buku la macitidwe a mafumu a Yuda? 29Masiku ace Farao-Neko mfumu ya Aigupto anakwerera mfumu ya Asuri ku mtsinje wa Firate; Ddipo mfumu Yosiya anaturuka kuponyana naye, koma anapha Yosiya ku Megido, atamuona. 30Ndipo anyamata ace anamtengera wakufa m'gareta, nabwera naye ku Yerusalemu kucokera ku Megido, namuika m'manda ace ace. Ndipo anthu a m'dziko anatenga Yoahazi mwana wa Yosiya, namdzoza, namlonga ufumu m'malo mwa atate wace.
Yoahazi, Yoyakimu ndi Yoyakini mafumu oipa a Yuda.
31Yoahazi anali wa zaka makumi awiri mphambu zitatu polowa ufumu wace, nakhala mfumu miyezi itatu m'Yerusalemu ndi dzina la mace ndiye Hamutali mwana wa Yeremiya wa ku Libina. 32Nacita iye coipa pamaso pa Yehova, monga umo monse adacita makolo ace. 33Ndipo Faraoneko anammanga m'Ribila, m'dziko la Hamati; kuti asacite ufumu m'Yerusalemu; nasonkhetsa dzikoli msonkho wa matalente zana limodzi la siliva, ndi talente limodzi la golidi. 34Ndipo Farao-Neko analonga ufumu Eliyakimu mwana wa Yosiya, m'malo mwa Yosiya atate wace, nasanduliza dzina lace likhale Yoyakimu; koma anapita naye Yoahazi, nafika iye m'Aigupto, nafa komweko. 35Ndipo Yoyakimu anapereka siliva ndi golidi kwa Farao, koma anasonkhetsa dzikoli lipereke ndalamazi; monga mwa lamulo la Farao anasonkhetsa anthu a m'dziko siliva ndi golidi, yense monga mwa kuyesedwa kwace, kuzipereka kwa Farao-Neko.
36Yoyakimu anali wa zaka makumi awiri ndi zisanu polowa ufumu wace, nakhala mfumu zaka khumi ndi cimodzi m'Yerusalemu; ndi dzina la mace ndiye Zebida mwana wa Pedaya wa Ruma. 37Nacita iye coipa pamaso pa Yehova, monga mwa zonse adazicita makolo ace.

©The Bible Society of Malawi, 1992

1Masiku ace Nebukadinezara mfumu ya ku Babulo anakwerako,
Yoyakimu nagwira mwendo wace zaka zitatu; pamenepo
anatembenuka nampandukira. 2Ndipo Yehova anamtumizira magulu
a Akasidi, ndi magulu a Aaramu, ndi magulu a Amoabu, ndi magulu
a ana a Amoni, nawatumiza pa Yuda kuliononga, monga mwa mau a
Yehova: adawanena ndi dzanja la atumiki ace aneneriwo. 3Zedi ici
cinadzera Yuda mwa lamulo la Yehova, kuwacotsa pamaso pace,
cifukwa ca zolakwa za Manase, monga mwa zonse
anazicita; 4ndiponso cifukwa ca mwazi wosacimwa adaukhetsa;
popeza anadzaza Yerusalemu ndi mwazi wosacimwa; ndipo Yehova
sanafuna kukhululukira. 5Macitidwe ena tsono a Yoyakimu, ndi
zonse anazicita, sizilembedwa kodi m'buku la macitidwe a mafumu
a Yuda? 6Nagona Yoyakimu ndi makolo ace, ndipo Yoyakini mwana
wace anakhala mfumu m'malo mwace. 7Koma mfumu ya Aigupto
sinabwerezanso kuturuka m'dziko lace, pakuti mfumu ya Babulo
idalanda kuyambira ku mtsinje wa Aigupto kufikira ku mtsinje Firate,
ndilo lonse anali nalo mfumu ya Aigupto.

Ayamba kutengedwa ukapolo kumka ku Babulo

8Yoyakini anali wa zaka khumi mphambu zisanu ndi zitatu polowa
iye ufumu wace, nakhala mfumu m'Yerusalemu miyezi itatu; ndi
dzina la mace ndiye Nehusita mwana wa Elinatani wa ku
Yerusalemu. 9Nacita iye coipa pamaso pa Yehova, monga umo
monse adacita atate wace. 10Nthawi ija anyamata a
Nebukadinezara mfumu ya Babulo anakwerera Yerusalemu,
naumangira mudziwo misasa. 11Nafika Nebukadinezara mfumu ya
Babulo kumudzi, ataumangira misasa anyamata ace, 12ndipo
Yoyakini mfumu ya Yuda anaturukira kwa mfumu ya Babulo, iye ndi
mace, ndi anyamata ace, ndi akalonga ace, ndi adindo ace; mfumu
ya Babulo nimtenga caka cacisanu ndi citatu ca ufumu
wace. 13Naturutsa kucotsa komweko cuma conse ca nyumba ya
Yehova, ndi cuma ca nyumba ya mfumu, naduladula zipangizo
zonse zagolidi adazipanga Solomo mfumu ya Israyeli m'Kacisi wa
Yehova, monga Yehova adanena. 14Nacoka nao a m'Yerusalemu
onse, ndi akalonga onse, ndi ngwazi zonse, ndiwo andende zikwi
khumi, ndi amisiri onse, ndi osula onse; sanatsala ndi mmodzi
yense, koma anthu osauka okha okha a m'dziko. 15Nacoka naye
Yoyakini kumka naye ku Babulo, ndi mace wa mfumu, ndi akazi a
mfumu, ndi adindo ace, ndi omveka a m'dziko; anacoka nao
andende ku Yerusalemu kumka nao ku Babulo. 16Ndi anthu
amphamvu onse, ndiwo zikwi zisanu ndi ziwiri, ndi amisiri, ndi
osula cikwi cimodzi, onsewo acamuna oyenera nkhondo, omwewo
mfumu ya Babulo anadza nao andende ku Babulo. 17Ndipo mfumu

ya Babulo analonga Mataniya mbale wa atate wace akhale mfumu m'malo mwace, nasanduliza dzina lace likhale Zedekiya.

Zedekiya mfumu yotsiriza ya Yuda

18Zedekiya anali wa zaka makumi awiri mphambu cimodzi polowa ufumu wace, nakhala mfumu zaka khumi ndi cimodzi m'Yerusalemu; ndi dzina la mace ndiye Hamutala mwana wa Yeremiya wa ku Libina. 19Nacita iye coipa pamaso pa Yehova, monga mwa zonse adacita Yoyakimu. 20Pakuti mwa mkwiyo wa Yehova zonse zidacitika m'Yerusalemu ndi m'Yuda, mpaka adawataya pamaso pace; ndipo Zedekiya anapandukira mfumu ya Babulo.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Yerusalemu apasulidwa, anthu natengedwa kunka ku Babulo

1Ndipo kunali caka cacisanu ndi cinai ca ufumu wace, mwezi
wakhumi, tsiku lakhumi la mwezi, Nebukadinezara mfumu ya
Babulo, iye ndi khamu lace lonse anadzera Yerusalemu,
naumangira misasa, naumangira timalinga mouzinga. 2Ndipo
mudziwo unazingidwa ndi timalinga mpaka caka cakhumi ndi
cimodzi ca mfumu Zedekiya. 3Tsiku lacisanu ndi cinai la mwezi
wacinai njala idakula m'mudzimo, panalibe cakudya kwa anthu a
m'dzikomo. 4Pamenepo linga la mudziwo linagamulidwa, nathawira
ankhondo onse usiku, njira ya ku cipata ca pakati pa makoma
awiri, iri ku munda wa mfumu; Akasidi tsono anali pamudzi
pouzinga; nimuka mfumu pa njira ya kucidikha. 5Koma nkhondo ya
Akastdi inalondola mfumu, niipeza m'zidikha za Yeriko; koma
nkhondo yace yonse inambalalikira. 6Ndipo anaigwira mfumu,
nakwera nayo kwa mfumu ya Babulo ku Ribila, naweruza mlandu
wace. 7Napha ana a Zedekiya pamaso pace, namkolowola
Zedekiya maso ace, nammanga ndi maunyolo amkuwa, namuka
nave ku Babulo. 8Ndipo mwezi wacisanu, tsiku lacisanu ndi ciwiri la
mweziwo, ndico caka cakhumi mphambu cisanu ndi cinai ca
mfumu Nebukadinezara mfumu ya Babulo, Nebuzaradani mkuru
wa olindirira, ndiye mnyamata wa mfumu ya Babulo, anadza ku
Yerusalemu, 9natentha nyumba ya Yehova, ndi nyumba ya mfumu,
ndi nyumba zonse za m'Yerusalemu; ndi nyumba zonse zazikuru
anazitentha ndi moto. 10Ndi khamu lonse la Akasidi linali ndi mkuru
wa olindirira linagumula linga la Yerusalemu louzinga. 11Ndi anthu
otsalira m'mudzi, ndi opanduka akuthawira kwa mfumu ya Babulo,
ndi aunyinji otsalira, Nebuzaradani mkuru wa olindirira anamuka
nao andende. 12Koma mkuru wa olindirira anasiya osaukadi a
m'dziko akhale osunga minda yampesa, ndi alimi, 13Ndipo
zoimiritsa zamkuwa zinali m'nyumba ya Yehova, ndi maphaka ace,
ndi thawale lamkuwa, zinali m'nyumba ya Yehova, Akasidi
anazithyolathyola, natenga mkuwa wace kumka nao ku
Babulo. 14Nacotsanso miphika, ndi zoolera, ndi zozimira nyali, ndi
zipande, ndi zipangizo zonse zamkuwa zimene anatumikira
nazo. 15Ndi zoparira moto, ndi mbale zowazira za golidi yekha
yekha, ndi zasiliva yekha yekha, mkuru wa asilikari
anazicotsa. 16Nsanamira ziwiri, thawale limodzi, ndi maphakawo
adazipangira nyumba ya Yehova Solomo, mkuwa wa zipangizo izi
zonse sanakhoza kuyesa kulemera kwace. 17Msinkhu wace wa
nsanamira imodzi ndiwo mikono khumi mphambu isanu ndi itatu,
ndi pamwamba pace mutu wamkuwa; ndi msinkhu wace wa
mutuwo ndiwo mikono itatu, ndi ukonde, ndi makangaza pamutu
pouzinga, zonse zamkuwa; ndi nsanamira inzace inali nazo

zomwezo pamodzi ndi ukonde. 18Ndipo mkuru wa olindirira
anatenga Seraya wansembe wamkulu, ndi Zefaniya wansembe
waciwiri, ndi olindira pakhomo atatu; 19natenga m'mudzimo
mdindo woikidwa woyang'anira ankhondo; ndi anthu asanu a iwo
openya nkhope ya mfumu opezeka m'mudzimo; ndi mlembi,
kazembe wa nkhondo wolembera anthu a m'dziko; ndi anthu a
m'dziko makumi asanu ndi limodzi opezeka m'mudzimo. 20Ndipo
Nebuzaradani mkuru wa olindirira anawatenga, napita nao kwa
mfumu ya Babulo ku Ribila. 21Niwakantha mfumu ya Babulo,
niwaphera ku Ribila m'dziko la Hamati. Motero anamuka nao Ayuda
andende kuwacotsa m'dziko lao.

Gedaliya wolamulira m'Yerusalemu aphedwa ndi Ismayeli

22Koma kunena za anthu otsalira m'dziko la Yuda, amene
adawasiya Nebukadinezara mfumu ya Babulo, iyeyu anamuika
Gedaliya mwana wa Ahikamu mwana wa Safani akhale
wowalamulira.
23Ndipo pamene anamva akazembe onse a makamu, iwo ndi anthu
ao, kuti mfumu ya Babulo adaika Gedaliya wowalamulira, anadza
kwa Gedaliya ku Mizipa, ndiwo Ismayeli mwana wa Netaniya, ndi
Yohanana mwana wa Kareya, ndi Seraya mwana wa Tanumeti wa
ku Netofa, ndi Yazaniya mwana wa Mmakati, iwo ndi anthu ao
omwe. 24Nawalumbirira Gedaliya iwo ndi anthu ao, nanena nao,
Musamaopa anyamata a Akasidi; khalani m'dziko; tumikirani
mfumu ya Babulo, ndipo kudzakukomerani. 25Koma kunali mwezi
wacisanu ndi ciwiri anadza Ismayeli mwana wa Netaniya mwana
wa Elisama, wa mbumba yacifumu, ndi anthu khumi pamodzi
naye, nakantha Gedaliya; nafa iye, ndi Ayuda, ndi Akasidi okhala
naye ku Mizipa. 26Pamenepo ananyamuka anthu onse ang'ono ndi
akuru, ndi akazembe a makamu, nadza ku Aigupto; pakuti anaopa
Akasidi.
27Ndipo kunali caka ca makumi atatu mphambu zisanu ndi ziwiri ca
kumtenga ndende Yoyakini mfumu ya Yuda, mwezi wakhumi ndi
ziwiri, tsiku la makumi awiri mphambu asanu ndi awiri la mwezi,
Evili Merodaki mfumu ya Babulo anamuweramutsa mutu wace wa
Yoyakini mfumu ya Yuda aturuke m'kaidi, caka colowa iye ufumu
wace; 28nakamba naye zokoma, namkweza mpando wace
waulemu upose mipando ya mafumu anali pamodzi naye
m'Babulo. 29Nasintha zobvala zace za m'kaidi, namadya iye mkate
pamaso pace masiku onse a moyo wace. 30Ndi kunena za cakudya
cace, panali cakudya cosalekeza copatsidwa kwa iye ndi mfumu,
tsiku Uri lonse gawo lace, masiku onse a moyo wace.

©The Bible Society of Malawi, 1992

1 Chronicles

1 Mbiri 1

Maina a makolo kuyambira Adamu kufikira adzukulu a Nowa

1ADAMU, Seti, Enosi, 2Kenani, Mahalaheli, Yaredi, 3Enoki, Metusela,
Lameki, 4Nowa, Semu, Hamu, ndi Yafeti.
5Ana a Yafeti: Gomeri, ndi Magogi, ndi Madai, ndi Yavani, ndi
Tubala, ndi Meseki, ndi Tirasi. 6Ndi ana a Gomeri: Asikenazi, Difati,
ndi Togarima. 7Ndi ana a Yavani: Elisa, ndi Tarisisa, Kitimu, ndi
Rodanimu.
8Ana a Hamu: Kusi, ndi Mizraimu, Puti, ndi Kanani. 9Ndi ana a Kusi:
Seba, ndi Havila, ndi Sabita, ndi Rama, ndi Sabteka. Ndi ana a
Rama: Seba, ndi Dedani. 10Ndi Kusi anabala Nimmdi; iye
anayamba kukhala wamphamvu pa dziko. 11Ndi Mizraimu anabala
Aludi, ndi Aanami, ndi Alehabi, ndi Anaftuki, 12ndi Apatrusi, ndi
Akasluki, (kumene anafuma Afilisti), ndi Akafitori. 13Ndi Kanani
anabala Zidoni mwana wace woyamba, ndi Heti, 14ndi Ayebusi, ndi
Aamori, ndi Agirigasi, 15ndi Ahivi, ndi Aariki, ndi Asini, 16ndi
Aarivadi, ndi Azemari, ndi Ahamati.
17Ana a Semu: Elamu, ndi Asuri, ndi Aripakisadi, ndi Ludi, ndi
Aramu, ndi Uzi, ndi Huli, ndi Geteri, ndi Meseki. 18Ndi Aripakisadi
anabala Sela; ndi Sela anabala Eberi. 19Ndi Eberi anabala ana
amuna awiri, dzina la winayo ndiye Pelegi, popeza masiku ace
dziko linagawanika; ndi dzina la mbale wace ndiye
Yokitani. 20Ndipo Yokitani anabala Almodadi, ndi Selefi, ndi
Hazaramaveti, ndi Yera; 21ndi Hadoramu, ndi Uzali, ndi Dikila; 22ndi
Ebala, ndi Abimaele, ndi Seba, 23ndi Ofiri, ndi Havila, ndi Yobabi.
Awa onse ndiwo ana a Yokitani.

Makolo kuyambira Semu mpaka adzukulu a Abrahamu

24Semu, Aripakisadi, Sela; 25Eberi, Pelegi, Reu, 26Serugi, Nahori,
Tera; 27Abramu, (ndiye Abrahamu). 28Ana a Abrahamu: Isake, ndi
Ismayeli.
29Mibadwo yao ndi awa; woyamba wa Ismayeli Nebayoti; ndi
Kedara ndi Adibeli, ndi Mibisamu, 30Misma, ndi Duma
Masa, 31Hadada, ndi Tema, Nafisi, ndi Kedema. Awa ndi ana a
Ismayeli.
32Ndi ana a Ketura mkazi wamng'ono wa Abrahamu anabala
Zimiramu, ndi Yokisani, ndi Medani, ndi Midyani, ndi Isibaki, ndi
Sua. Ndi ana a Yokisani: Seba, ndi Dedani. 33Ndi ana a Midyani:
Efa, ndi Eferi, ndi Hanoki, ndi Abida, ndi Elidaa. Awa onse ndiwo
ana a Ketura.
34Ndipo Abrahamu anabala Isake. Ana a Isake: Esau, ndi Israyeli.
35Ana a Esau: Elifazi, Reueli, ndi Yeuzi, ndi Yolamu, ndi Kora. 36Ana
a Elifazi: Teani, ndi Omara, Zefi, ndi Gatamu, Kenazi, ndi Timna, ndi

Amaleki. 37Ana a Reueli: Nahati, Zera, Sama, ndi Miza. 38Ndi ana a
Seiri: Lotani, ndi Sobala, ndi Zibeoni, ndi Ana, ndi Disoni, ndi Ezeri,
ndi Disani. 39Ndi ana a Lotani: Hori, ndi Homamu; ndipo Timna
ndiye mlongo wace wa Lotani. 40Ana a Sobala: Abiani, ndi
Manahati, ndi Ebala, Sefi, ndi Oramu. Ndi ana a Zibeoni: Aiya ndi
Ana. 41Mwana wa Ana: Disoni. Ndi ana a Disoni: Hamirani, ndi
Esibani, ndi Itrani, ndi Kerani. 42Ana a Ezeri: Bilani, ndi Zavani, ndi
Yakani. Ana a Disani: Uzi, ndi Arani. 43Mafumu tsono akucita ufumu
m'dziko la Edomu, pakalibe mfumu wakucita ufumu pa ana a
Israyeli, ndiwo Bela mwana wa Beori; ndi dzina la mudzi wace ndilo
Dinaba. 44Ndipo anafa Bela; ndi Yobabi mwana wa Zera wa ku
Bozra anakhala mfumu m'malo mwace. 45Namwalira Yobabi; ndi
Husamu wa ku dziko la Atemani anakhala mfumu m'malo
mwace. 46Namwalira Husamu; ndi Hadada mwana wa Bedadi,
amene anakantha Midyani ku thengo la Moabu, anakhala mfumu
m'malo mwace; ndi dzina la mudzi wace ndi Aviti. 47Namwalira
Hadada; ndi Samla wa ku Masereka anakhala mfumu m'malo
mwace. 48Namwalira Samla: ndi Sauli wa ku Rehoboti ku nyanja
anakhala mfumu m'malo mwace. 49Namwalira Sauli; ndi
Baalahanani mwana wa Akiboro anakhala mfumu m'malo
mwace. 50Namwalira Baalahanani; ndi Hadada anakhala mfumu
m'malo mwace; ndipo dzina la mudzi wace ndi Pai; ndi dzina la
mkazi wace ndiye Mehetabele mwana wamkazi wa Matradi mwana
wamkazi wa Mezahabu. 51Namwalira Hadada. Ndipo mafumu a
Edomu ndiwo mfumu Timna, mfumu Aliya, mfumu Yeteti; 52mfumu
Oholibama, mfumu Bla, mfumu Pimoni; 53mfumu Kenazi, mfumu
Temani, mfumu Mizibara; 54mfumu Magadieli, mfumu Iramu. Awa
ndi mafumu a Edomu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

2 Chronicles

2 Mbiri 1

Solomo apereka nsembe ku Gibeoni

1NDIPO Solomo mwana wa Davide analimbikitsidwa m'ufumu
wace, ndipo Yehova Mulungu wace anali naye, namkuza
kwakukuru. 2Ndipo Solomo analankhula ndi Aisrayeli onse, ndi
akuru a zikwi ndi a mazana, ndi kwa oweruza, ndi kwa kalonga ali
yense wa Israyeli, akuru a nyumba za makolo. 3Ndipo Solomo ndi
khamu lonse pamodzi naye anamuka ku msanje wa ku Gibeoni;
pakuti kumeneko kunali cihema cokomanako ca Mulungu
adacimanga Mose mtumiki wa Yehova m'cipululu. 4Koma likasa la
Mulungu Davide adakwera nalo kucokera ku Kiriyati Yearimu
kumka kumene Davide adalikonzeratu malo; pakuti adaliutsiratu
hema ku Yerusalemu. 5Guwa la nsembe lomwe lamkuwa,
adalipanga Bezaleli mwana wa Uri mwana wa Huri linali komweko,
ku khomo la kacisi wa Yehova; ndipo Solomo ndi khamulo
anafunako. 6Nakwerako Solomo ku guwa la nsembe pamaso pa
Yehova linali ku cihema cokomanako, napereka pamenepo nsembe
zopsereza cikwi cimodzi.

Solomo apempha nzeru kwa Mulungu

7Usiku womwewo Mulungu anaonekera kwa Solomo, nati kwa iye,
Pempha comwe ndikupatse. 8Nati Solomo kwa Mulungu, Mwacitira
Davide atate wanga zokoma zambiri, ndipo mwandiika mfumu
m'malo mwace. 9Tsopano, Yehova Mulungu, likhazikike lonjezano
lanu la kwa Davide atate wanga; pakuti mwandiika mfumu ya
anthu akucuruka ngati pfumbi lapansi. 10Mundipatse tsono nzeru
ndi cidziwitso, kuti ndituruke ndi kulowa pamaso pa anthu awa;
pakuti angathe ndani kuweruza anthu anu awa ambiri? 11Ndipo
Mulungu anati kwa Solomo, Popeza cinali mumtima mwako ici,
osapempha cuma, akatundu, kapena ulemu, kapena moyo wa iwo
akudana nawe, osapemphanso masiku ambiri; koma
wadzipemphera nzeru ndi cidziwitso, kuti uweruze anthu anga
amene ndakuika ukhale mfumu yao, 12nzeru ndi cidziwitso
zipatsidwa kwa iwe, ndidzakupatsanso cuma, ndi akatundu, ndi
ulemu, zotere zonga sanakhala nazo mafumu akale usanakhale
iwe, ndi akudza pambuyo pako sadzakhala nazo
zotero. 13Momwemo Solomo anadza ku Yerusalemu kucokera ku
msanje uli ku Gibeoni, ku khomo la cihema cokomanako; ndipo
anacita ufumu pa Israyeli.

Magareta ndi apakavalo a Solomo

14Ndipo Solomo anasonkhanitsa magareta ndi apakavalo, nakhala
nao magareta cikwi cimodzi mphambu mazana anai, ndi apakavalo
zikwi khumi ndi ziwiri; nawaika m'midzi ya magareta ndi kwa

mfumu ku Yerusalemu. 15Ndipo mfumu inatero kuti siliva ndi golidi
zikhale m'Yerusalemu ngati miyala, ndi kuti mikungudza icuruke
ngati mikuyu yokhala kucidikha. 16Ndi akavalo amene Solomo anali
nao anafuma ku Aigupto; amalonda a mfumu anawalandira
magulu magulu, gulu liri lonse mtengo wace. 17Ndipo anatenga
naturuka nalo gareta ku Aigupto mtengo wace masekeli a siliva
mazana asanu ndi limodzi, ndi kavalo mtengo wace zana limodzi
mphambu makumi asanu; momwemo anawaturutsira mafumu
onse a Ahiti, ndi mafumu a Aramu, ndi dzanja lao.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Solomo apangana ndi Hiramu za mirimo ya Kacisi

1Ndipo a Solomo anati alimangire dzina la Yehova nyumba,
ndiponso nyumba ya ufumu wace. 2Nawerenga Solomo amuna
zikwi khumi mphambu makumi asanu ndi limodzi osenza mirimo,
ndi amuna zikwi makumi asanu ndi atatu otema mitengo m'mapiri,
ndi zikwi zitatu mphambu mazana asanu ndi limodzi
kuwayang'anira. 3Ndipo Solomo anatumiza kwa Huramu mfumu ya
Turo, ndi kuti, Monga momwe munacitira Davide atate wanga, ndi
kumtumizira mikungudza yommangira nyumba yokhalamo,
mundicitire ine momwemo. 4Taonani, nditi ndilimangire dzina la
Yehova Mulungu wanga nyumba, kumpatulira iyo, ndi kufukiza
pamaso pace zonunkhira za pfungo lokoma, ndiyo ya mkate
woonekera wacikhalire, ndi ya nsembe zopsereza, m'mawa ndi
madzulo, pamasabata, ndi pokhala mwezi, ndi pa madyerero oikika
a Yehova Mulungu wathu. Ndiwo macitidwe osatha
m'Israyeli. 5Ndipo nyumba nditi ndimangeyi ndi yaikuru; pakuti
Mulungu wathu ndiye wamkuru woposa milungu yonse. 6Koma ali
nayo mphamvu ndani yakummangira Iye nyumba, popeza thambo
lam'mwambamwamba silimfikira? ndine yani ine tsono, kuti
ndimmangire nyumba, koma kumfukizira cofukiza ndiko? 7Ndipo
tsono munditumizire munthu wa luso lakucita ndi golidi, ndi siliva,
ndi mkuwa, ndi citsulo, ndi thonje lofiirira, ndi lofiira, ndi lamadzi,
wakudziwa kuzokota zozokota ziri zonse, akhale ndi amuna aluso
okhala ndi ine m'Yuda ndi m'Yerusalemu, amene Davide atate
wanga anawakonzeratu. 8Munditumizirenso mitengo
yamikungudza, ndi yamlombwa, ndi yambawa, ya ku Lebano;
pakuti ndidziwa kuti anyamata anu adziwa kutema mitengo
m'Lebano; ndipo taonani, anyamata anga adzakhala ndi anyamata
anu, 9ndiko kundikonzera mitengo yambirimbiri; pakuti nyumbayi
nditi ndiimange idzakhala yaikuru ndi yodabwitsa. 10Ndipo taonani,
ndidzawapatsa anyamata anu otema akulikha mitengo miyeso ya
tirigu wopuntha zikwi makumi awiri, ndi miyeso ya barele zikwi
makumi awiri, ndi mitsuko yaikuru ya vinyo zikwi makumi awiri, ndi
mitsuko yaikufu ya mafuta zikwi makumi awiri. 11Ndipo Huramu
mfumu ya Turo anayankha ndi kulembera, natumiza kalatayo kwa
Solomo, ndi kuti, Powakonda anthu ace Yehova anakulongani
mfumu yao. 12Huramu anatinso, Alemekezedwe Yehova Mulungu
wa Israyeli, amene analenga kumwamba ndi dziko lapansi,
nampatsa mfumu Davide mwana waluso, wodziwa nzeru ndi
waluntha, ammangire Yehova nyumba, ndiponso nyumba ya
ufumu wace. 13Ndipo tsono ndatumiza munthu waluso wokhala
Ralo, luntha, Huramu Abi, 14ndiye mwana wa munthu wamkazi wa
ana akazi a Dani, ndipo atate wace ndiye munthu wa ku Turo,

wodziwa kucita ndi golidi, ndi siliva, ndi mkuwa, ndi citsulo, ndi mwala, ndi mitengo, ndi thonje lofiirira, ndi lamadzi, ndi bafuta la thonje losansitsa ndi lofiira, ndi kuzokota mazokotedwe ali onse, ndi kulingirira copanga ciri conse; kuti ampatse pokhala pamodzi ndi aluso anu, ndi aluso a mbuye wanga Davide atate wanu. 15Ndipo tsono tirigu ndi barele, mafuta ndi vinyo, mbuye wanga wanenazi, azitumize kwa anyamata ace; 16ndipo ife tidzatema mitengo ku Lebano monga mwa kusowa kwanu konse; ndipo tidzabwera nayo kwa inu yoyandamitsa paphaka kufikira ku Yopa; ndipo inu mudzakwera nayo ku Yerusalemu. 17Ndipo Solomo anawerenga alendo Onse okhala m'dziko la Israyeli, monga mwa mawerengedwe aja atate wace Davide adawawerenga nao, nawapeza afikira zikwi zana limodzi mphambu makumi asanu kudza zitatu ndi mazana asanu ndi limodzi. 18Ndipo anaika zikwi makumi asanu ndi awiri za iwowa asenze mirimo, ndi zikwi makumi asanu ndi atatu ateme m'mapiri, ndi akapitao zikwi zitatu mphambu mazana asanu ndilimodzi agwiritse anthu nchito.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Mamangidwe a Kacisi

1Pamenepo Solomo anayamba kumanga nyumba ya Yehova ku
Yerusalemu, m'phiri la Moriya, kumene Mulungu anaonekera kwa
Davide atate wace, pamalo pamene Davide anakonzeratu pa
dwale la Orinani Myebusi. 2Nayamba kumanga tsiku laciwiri la
mwezi waciwiri, caka cacinai ca ufumu wace. 3Ndipo maziko
adawaika Solomo akumangapo nyumba ya Mulungu ndi awa: utali
wace, kuyesa mikono monga mwa muyeso wakale, ndiwo mikono
makumi asanu ndi limodzi, ndi kupingasa kwace mikono makumi
awiri. 4Ndi likole linali kukhomo kwa nyumba, m'litali mwace
monga mwa kupingasa kwa nyumba munali mikono makumi awiri,
ndi msinkhu wace zana limodzi mphambu makumr awiri; ndipo
analikuta m'katimo ndi golidi woona. 5M'nyumba yaikuru tsono
anacinga ndi mitengo yamlombwa, imene anaikuta ndi golidi
wabwino, nalembapo ngati migwalangwa ndi maunyolo. 6Ndipo
anakuta nyumba ndi miyala ya mtengo wace; ndi golidi wace ndiye
golidi wa Parivaimu. 7Anamamatizanso kacisi, mitanda, ziundo, ndi
makoma ace, ndi zitseko zace, ndi golidi; nalemba akerubi
pamakoma. 8Ndipo anamanga malo opatulikitsa, m'litali mwace
monga mwa kupingasa kwa nyumba mikono makumi awiri, ndi
kupingasa kwace mikono makumi awiri; naikuta ndi golidi wabwino
wakufikira matalente mazana asanu ndi limodzi. 9Ndi kulemera
kwace kwa misomali ndiko masekeli makumi asanu a golidi. Ndipo
anazikuta ndi golidi zipinda zosanjikizana. 10Ndipo m'malo
opatulikitsa anapanga akerubi awiri, anacita osema, nawakuta ndi
golidi. 11Ndi mapiko a akerubi m'litali mwace ndimo mikono
makumi awiri; phiko la kerubi mmodzi mikono isanu, lojima khoma
la nyumba; ndi phiko linzace mikono isanu, lokhudzana nalo phiko
la kerubi wina. 12Ndi phiko la kerubi wina mikono isanu lojima
khoma la nyumba, ndi phiko linzace mikono isanu lolumikizana ndi
phiko la kerubi wina. 13Mapiko a akerubi awa anafunyululika
mikono makumi awiri; ndipo anaima ndi mapazi ao, ndi, nkhope
zao zinaloza kukhomo. 14Ndipo anaomba nsaru yocinga ya thonje
lamadzi, ndi lofiirira, ndi lofiira, ndi bafuta wa thonje losansitsa,
naomberamo akerubi. 15Ndipo anapanga ku khomo la nyumba
nsanamira ziwiri za mikono makumi atatu mphambu ziwiri; ndi
mutu unakhala pamwamba pa iri yonse ndiwo mikono
isanu. 16Napanga maunyolo onga a m'moneneramo, nawamanga
pa mitu ya nsanamirazi, napanga makangaza zana limodzi,
nawamanga pamaunyolo. 17Ndipo anaimiritsa nsanamirazo
pakhomo pa Kacisi; imodzi ku dzanja lamanja, ndi inzace ku dzanja
lamanzere; nalicha dzina la iyi ya ku dzanja lamanja Yakini, ndi
dzina la iyi ya ku dzanja lamanzere Boazi.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Guwa la nsembe ndi thawale lamkawa ndi zipangizo zonse zina

1Anapanganso guwa la nsembe lamkuwa, m'litali mwace mikono
makumi awiri, ndi kupingasa kwace mikono makumi awiri, ndi
msinkhu wace mikono khumi. 2Anayenganso thawale losungunula
la mikono khumi kukamwa, lozunguniza, ndi msinkhu wace mikono
isanu; ndi cingweca mikono makumi atatu cinalizunguniza. 3Ndi
pansi pace panali mafanziro a ng'ombe zakulizinga khumi ku
mkono umodzi, zakuzinga thawalelo pozungulira pace. Ng'ombezo
zinali m'mizere iwiri, zinayengeka poyengedwa
thawalelo. 4Linasanjikika pa ng'ombe khumi ndi ziwiri, zitatu
zinapenya kumpoto, ndi zitatu zinapenya kumadzulo, ndi zitatu
zinapenya kumwela, ndi zitatu zinapenya kum'mawa; ndi thawale
linasanjikika pamwamba pao, ndi nkholo zao zinayang'anana. 5Ndi
kucindikira kwace kunanga cikhato, ndi mlomo wace unasadamuka
ngati mlomo wa comwera, ngati luwa la kakombo; analowamo
madzi a mitsuko yaikuru zikwi zitatu. 6Anapanganso mbiya
zamphwamphwa khumi, naika zisanu ku dzanja lamanja, ndi
zisanu ku dzanja lamanzere, kutsukiramo; za nsembe yopsereza
anazitsuka m'menemo; koma thawale ndi la ansembe
kusambiramo. 7Ndipo anapanga zoikapo nyali khumi zagolidi,
monga mwa ciweruzo cace; naziika m'Kacisi, zisanu ku dzanja
lamanja, ndi zisanu ku dzanja lamanzere. 8Anapanganso magome
khumi, nawaika m'Kacisi, asanu ku dzanja lamanja, ndi asanu ku
dzanja lamanzere. Napanga mbale zowazira zana limodzi
zagolidi. 9Anamanganso bwalo la ansembe, ndi bwalo lalikuru, ndi
zitseko za kubwalo, nakuta zitseko zace ndi mkuwa. 10Ndipo anaika
thawalelo ku dzanja lamanja la nyumba kum'mawa
cakumwela. 11Ndipo Huramu anapanga miphika, ndi zoolera zace,
ndi mbale zowazira zace. Natsiriza Huramu nchito adaicitira
mfumu Solomo m'nyumba ya Mulungu: 12nsanamira ziwiri, ndi
zikhozo, ndi mitu iwiri inali pamwamba pa nsanamirazo, ndi
maukonde awiri akukuta zikho ziwiri za mitu iri pamwamba pa
nsanamirazo, 13ndi makangaza mazana anai a maukonde awiri wa;
mizere iwiri ya makangaza ya ukonde uli wonse, akukuta zikho
ziwiri za mitu, inali pa nsanamirazo. 14Anapanganso maphaka,
napanga mbiya zamphwamphwa khumi pamwamba pa
maphaka; 15thawale limodzi ndi ng'ombe khumi ndi ziwiri pansi
pace. 16Miphika yomwe, ndi zoolera, ndi mitungo, ndi zipangizo
zace zonse, Huramu Abi anazipangira mfumu Solomo, kuzipangira
nyumba ya Yehova, za mkuwa wonyezimira. 17Mfumuyi inaziyenga
pa cidikha ca ku Yordano, m'dothi ladongo, pakati pa Sukoti ndi
Zereda. 18Ndipo Solomo anazipanga zipangizo izi zonse

zocurukadi, pakuti kulemera kwace kwa mkuwa
sikunayeseka. 19Solomo anapanganso zipangizo zonse zinali
m'nyumba ya Mulungu, guwa la nsembe lagolidi lomwe, ndi
magome oikapo mkate woonekera; 20ndi zoikapo nyali ndi nyali
zace za golidi woona, zakuunikira monga mwa cilangizo cace
cakuno ca moneneramo; 21ndi maluwa, ndi nyali, ndi mbano
zagolidi, ndiwo golidi wangwiro; 22ndi zozimira nyali, ndi mbale
zowazira, ndi zipande, ndi mbale za zofukiza za golidi woona; ndi
kunena za polowera m'nyumba, zitseko zace za m'katimo za malo
opatulikitsa, ndi zitseko za nyumbayi, ndiyo Kacisi, zinali zagolidi.

©The Bible Society of Malawi, 1992

1Momwemo zidatha nchito zonse Solomo adazicitira nyumba ya
Yehova. Ndipo Solomo anabwera nazo zopatulika zija za atate wace
Davide; naziika siliva, ndi golidi, ndi zipangizo zonse m'cuma ca
nyumba ya Mulungu.
Kuperekedwa kwa Kacisi.
2Pamenepo Solomo anasonkhanitsira akulu akulu a Israyeli, ndi
akuru onse a mafuko, ndi akalonga a nyumba za makolo a ana a
Israyeli, ku Yerusalemu, kukatenga likasa la cipangano ca Yehova
ku mudzi wa Davide ndiwo Zioni. 3Ndipo amuna onse a Israyeli
anasonkhana kwa mfumu kumadyerero anacitikawo, m'mwezi
wacisanu ndi ciwiri. 4Nadza akulu akulu onse a Israyeli, nanyamula
likasalo Alevi. 5Ndipo anakwera nalo likasa, ndi cihema
cokomanako, ndi zipangizo zonse zopatulika zinali m'cihemamo;
izizo ansembe Alevi anakwera nazo. 6Ndi mfumu Solomo ndi
khamu lonse la Israyeli losonkhana kwa iye anali kulikasa, naphera
nsembe, nkhosa ndi ng'ombe zosawerengeka kucuruka
kwace. 7Ndipo ansembe analowa nalo likasa la cipangano la
Yehova kumalo kwace m'moneneramo mwa kacisi, m'malo
opatulikitsa, pansi pa mapiko a akerubi. 8Pakuti akerubi
anafunyulula mapiko ao pa malo a likasa, ndi akerubi anaphimba
likasa ndi mphiko zace pamwamba pace. 9Ndipo zinatalikitsa
mphikozo, kuti nsonga za mphiko zidaoneka kulikasa cakuno ca
moneneramo, koma sizinaoneka kubwalo; ndipo ziri komweko
mpaka lero lino. 10Munalibe kanthu kena m'likasa, koma magome
awiri Mose anawaika m'mwemo ku Horebu, muja Yehova anacita
cipangano ndi ana a Israyeli poturuka iwo m'Aigupto. 11Ndipo
ansembe anaturuka m'malo opatulika, pakuti ansembe onse anali
komwe adadzipatula, osasunga magawidwe ao; 12Alevi omwe
akuyimba, onsewo ndiwo Asafu, Hemani, Yedutuni, ndi ana ao, ndi
abale ao obvala bafuta, ali nazo nsanje, ndi zisakasa, ndi azeze,
anaima kum'mawa kwa guwa la nsembe, ndi pamodzi nao
ansembe zana limodzi mphambu makumi awiri akuomba
malipenga. 13Ndipo kunali, pakucita limodzi amalipenga ndi
oyimba, kumveketsa mau amodzi akulemekeza ndi kuyamika
Yehova, ndi pakukweza mau ao pamodzi ndi malipenga, ndi nsanje,
ndi zoyimbira zina, ndi kulemekeza Yehova, ndi kuti, Pakuti Iye
ndiye wabwino, pakuti cifundo cace cikhala cikhalire; pamenepo
mtambo unadzaza nyumbayi, ndiyo nyumba ya Yehova; 14ndipo
ansembe sanakhoza kuimirira kutumikira cifukwa ca mtambowo;
pakuti ulemerero wa Yehova unadzaza nyumba ya Mulungu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Conena Solomo ndi pemphero lace popereka Kacisi

1Pamenepo Solomo anati, Yehova anati kuti adzakhala mu mdima
wandiweyani. 2Koma ndakumangirani nyumba yokhalamo, malo
okhazikika okhalamo Inu nthawi yosatha. 3Ndipo mfumu
inapotolokera nkhope yace, nidalitsa khamu lonse la Israyeli; ndi
khamu lonse la Israyeli linaimirira. 4Nati iye, Alemekezedwe
Yehova Mulungu wa Israyeli, wakunena m'kamwa mwace ndi
Davide atate wanga, nakwaniritsa: ndi manja ace, ndi
kuti, 5Kuyambira tsiku lakuturutsa Ine anthu anga m'dziko la
Aigupto, sindinasankha mudzi uli wonse m'mafuko onse a Israyeli,
kumangamo nyumba yokhalamo dzina langa, kapena kusankha
munthu ali yense akhale kalonga wa anthu anga Israyeli; 6koma
ndinasankha Yerusalemu, kuti dzina langa likhale komweko;
ndinasankhanso Davide akhale mfumu ya anthu anga
Israyeli. 7Ndipo Davide atate wanga anafuna mumtima mwace
kumangira dzina la Yehova Mulungu wa Israyeli nyumba. 8Koma
Yehova anati kwa Davide atate wanga, Popeza unafuna mumtima
mwako kulimangira dzina langa nyumba, unacita bwino kuti
unatero mumtima mwako; 9koma sudzandimangira nyumba ndiwe,
koma mwana wako wakudzaturuka m'cuuno mwako, Iyeyo
adzalimangira dzina langa nyumbayi. 10Ndipo Yehova wakhazikitsa
mau ace adanenawo, pakuti ndinauka ine m'malo mwa Davide
atate wanga, ndipo ndikhala pa mpando wacifumu wa Israyeli
monga analonjeza Yehova, ndipo ndamangira dzina la Yehova
Mulungu wa Israyeli nyumbayi. 11Ndipo ndalongamo likasa, muli
cipangano ca Yehova, anacicita ndi ana a Israyeli.
12Ndipo Solomo anaima ku guwa la nsembe la Yehova pamaso pa
khamu lonse la Israyeli, natambasula manja ace. 13Ndipo Solomo
adapanga ciunda camkuwa, m'litali mwace mikono isanu, ndi
kupingasa kwace mikono isanu, ndi msinkhu wace mikono itatu,
naciika pakati pa bwalo; ndipo anaima pamenepo, nagwada pa
maondo ace pamaso pa khamu lonse la Israyeli, natambasulira
manja ace kumwamba; 14nati, Yehova. Mulungu wa Israyeli, palibe
Mulungu ngati Inu, m'mwamba, kapena pa dziko lapansi,
wakusungira cipangano ndi cifundo akapolo anu akuyenda pamaso
panu ndi mtima wao wonse; 15inu amene mwasungira mtumiki
wanu Davide atate wanga cija mudamlonjezaci: inde munanena
ndi pakamwa panu, ndipo mwacita ndi dzanja lanu, monga momwe
muli lero lino. 16Ndipo tsopano, Yehova Mulungu wa Israyeli,
msungireni mtumiki wanu Davide cija mudamlonjezaco, ndi kuti,
Sadzakusowa munthu pamaso panga wakukhala pa mpando
wacifumu wa Israyeli; pokhapo ngati ana ako asamalira njira yao,
kuti ayende m'cilamulo canga, monga umo unayendera iwe

pamaso panga. 17Ndipo tsopano, Yehova Mulungu wa Israyeli, acitike mau anu amene munanena kwa Davide mtumiki wanu. 18Koma kodi nzoona kuti Mulungu akhala ndi anthu pa dziko lapansi? taonani, thambo, inde m'mwambamwamba, sizifikira inu, koposa kotani nanga nyumba iyi ndaimanga? 19Cinkana citero, labadirani pemphero la kapolo wanu, ndi pembedzero lace, Yehova Mulungu wanga, kumvera kupfuula ndi kupempha kwace, kumene kapolo wanu apempha pamaso panu; 20kuti maso anu atsegukire nyumba iyi usana ndi usiku, malo amene munanenerako kuti mudzaikako dzina lanu, kuti mumvere pemphero limene kapolo wanu adzapempha kuloza konkuno. 21Ndipo mverani mapembedzero a kapolo wanu ndi a anthu anu Israyeli, popemphera iwo kuloza konkuno; ndipo mumvere Inu m'Mwamba mokhala Inumo, ndipo pakumva Inu, mukhululikire. 22Munthu akacimwira mnansi wace, ndipo akamuikira lumbiro lakumlumbiritsa, ndipo akadzalumbira ku guwa lanu la nsembe, m'nyumba yino; 23pamenepo mumvere m'Mwamba, nimucite ndi kuweruzira akapolo anu, kumtsutsa woipayo, ndi kumbwezera chimo lace, ndi kulungamitsa wolungamayo, kumbwezera monga mwa cilungamo cace. 24Ndipo anthu anu Israyeli akawakantha mdani cifukwa ca kukucimwirani, nakabwerera iwowa ndi kubvomereza dzina lanu, ndi kupemphera, ndi kupembedzera pamaso panu m'nyumba yino; 25pamenepo mumvere Inu m'Mwamba, nimukhululukire chimo la anthu anu Israyeli, ndi kuwabwezera ku dziko limene munapatsa makolo ao. 26Mukatsekeka m'mwamba, mopanda mvula, cifukwa ca kukucimwirani; akapemphera iwo kuloza kumalo kuno, ndi kubvomereza dzina lanu, ndi kutembenuka kwa zoipa zao, pamene muwasautsa; 27pamenepo mumvere Inu m'Mwamba, nimukhululukire chimo la akapolo anu, ndi la anthu anu Israyeli, mutawalangiza njira, yokoma ayenera kuyendamo, nimutumizire mvula dziko lanu limene munapatsa anthu anu likhale colowa cao. 28Mukakhala njala m'dzikomo, mukakhala mliri, mukakhala cinsikwi, kapena cinoni, dzombe, kapena kapuce; akawamangira misasa adani ao, m'dziko la midzi yao; mukakhala mliri uli wonse, kapena nthenda iri yonse; 29pemphero ndi pembedzero liri lonse likacitika ndi munthu ali yense, kapena ndi anthu anu onse Aisrayeli, akadziwa yense cinthenda cace, ndi cisoni cace, nakatambasulira manja ace kuloza ku nyumba iyi; 30pamenepo mumvere m'Mwamba mokhala Inumo, nimukhululukire, ndi kubwezera ali yense monga mwa njira zace zonse, monga mudziwa mtima wace; pakuti Inu, Inu nokha, mudziwa mitima ya ana a anthu; 31kuti aope Inu, kuyenda m'njira zanu masiku onse akukhala iwo m'dziko limene munapatsa makolo athu. 32Ndiponso

kunena za mlendo wosakhala wa anthu anu Israyeli, akafumira ku dziko lakutari cifukwa ca dzina lanu lalikuru, ndi dzanja lanu lamphamvu, ndi mkono wanu wotambasuka; akadza iwowa ndi kupemphera kuloza ku nyumba iyi; 33pamenepo mumvere Inu m'Mwamba mokhala Inumo, nimumcitire mlendoyo monga mwa zonse akuitanirani; kuti mitundu yonse ya anthu a pa dziko lapansi adziwe dzina lanu, nakuopeni, monga amatero anthu anu Aisrayeli; ndi kuti adziwe kuti nyumba iyi ndamangayi ichedwa ndi dzina lanu. 34Akaturukira kunkhondo anthu anu kuyambana ndi adani ao, kutsata njira iri yonse muwatumiza; nakapemphera kwa Inu kuloza ku mudzi uwu munausankha, ndi nyumba iyi ndaimangira dzina lanu; 35pamenepo mumvere m'Mwamba pemphero lao ndi pembedzero lao, ndi kulimbitsa mlandu wao. 36Akacimwira Inu (pakuti palibe munthu wosacimwa), nimukakwiya nao, ndi kuwapereka kwa adani, kuti awatenge andende kumka nao ku dziko lakutali, kapena lapafupi; 37koma akalingirira m'mtima mwao kudziko kumene anawatengera andende, nakatembenuka, nakapembedzera Inu m'dziko la undende wao, ndi kuti, Tacimwa, tacita mphulupulu, tacita coipa; 38akabwerera kwa Inu ndi mtima wao wonse, ndi moyo wao wonse, m'dziko la undende wao, kumene adawatengera andende; nakapemphera kuloza ku dziko lao limene munapatsa makolo ao, ndi mudzi mudausankha, ndi kunyumba ndamangira dzina lanuyi; 39pamenepo mumvere Inu m'Mwamba mokhala Inumo pemphero lao ndi pembedzero lao, ndi kulimbitsa mlandu wao; nimukhululukire anthu anu amene anakucimwirani. 40Tsopano Mulungu wanga, maso anu akhale cipenyere, ndi makutu anu cimvere, pemphero locitika pamalo pano. 41Ndipo tsopano nyamukani, Yehova Mulungu, kudza kopumulira kwanu, Inu ndi likasa la mphamvu yanu; ansembe anu, Yehova Mulungu, abvale cipulumutso; ndi okondedwa anu akondwere nazo zabwino. 42Yehova Mulungu, musabweza nkhope ya wodzozedwa wanu, mukumbukile zacifundo za Davide mtumiki wanu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Cibvomerezo ca Yehova mwa moto ndi ulemerero wao wodzaza Kacisi

1Atatha tsono Solomo kupemphera, moto unatsika kumwamba,
nunyeketsa nsembe yopsereza, ndi nsembe zophera; ndipo
ulemerero wa Yehova unadzaza nyumbayi. 2Ndipo ansembe
sanakhoza kulowa m'nyumba ya Yehova, popeza ulemerero wa
Yehova unadzaza nyumba ya Yehova. 3Ndi ana onse a Israyeli
anapenyerera potsika motowo, ndi pokhala ulemerero wa Yehova
panyumbayi; nawerama nkhope zao pansi poyalidwa miyala,
nalambira, nayamika Yehova, nati, Pakuti Iye ndiye wabwino,
pakuti cifundo cace cikhala cikhalire. 4Pamenepo mfumu ndi anthu
onse anapereka nsembe pamaso pa Yehova. 5Ndipo mfumu
Solomo anapereka nsembe ya ng'ombe zikwi makumi awiri
mphambu ziwiri, ndi nkhosa zikwi, makumi awiri. Momwemo
mfumu ndi anthu onse anapereka nyumba ya Yehova. 6Naimirira
ansembe m'udikiro wao; ndi Alevi omwe ndi zoyimbira za Yehova,
adazipanga Davide mfumu kuyamika nazo Yehova, pakuti cifundo
cace cikhala cikhalire, polemekeza Davide mwa utumiki wao; ndi
ansembe anaomba malipenga pamaso pao, nakhala ciriri Israyeli
yense. 7Ndipo Solomo anapatula pakati pace pa bwalo liri
pakhomo pa nyumba ya Yehova; pakuti anapereka nsembe
zopsereza, ndi mafuta a nsembe zoyamika pomwepo; popeza
guwa la nsembe lamkuwa adalipanga Solomo linacepa kulandira
nsembe yopsereza, ndi nsembe yaufa, ndi mafuta. 8Nthawi
yomweyo Solomo anacita madyerero masiku asanu ndi awiri, ndi
Aisrayeli onse pamodzi naye, khamu lalikuru ndithu, kuyambira
polowera ku Hamati kufikira mtsinje wa ku Aigupto. 9Ndipo tsiku
lacisanu ndi citatu anacita msonkhano woletsa; popeza anacita
zakupereka guwa la nsembe masiku asanu ndi awiri, ndi
madyerero masiku asanu ndi awiri. 10Ndipo tsiku la makumi awiri
ndi citatu la mwezi wacisanu ndi ciwiri anawauza anthu apite ku
mahema ao, akusekera ndi kukondwera m'mtima mwao cifukwa ca
zokoma Yehova adawacitira Davide, ndi Solomo, ndi Aisrayeli
anthu ace.

Yehova aonekeranso kwa Solomo

11Momwemo Solomo anatsiriza nyumba ya Yehova, ndi nyumba ya
mfumu; ndipo ziri zonse zidalowa mumtima mwace mwa Solomo
kuzicita m'nyumba ya Yehova, ndi m'nyumba yace yace, anacita
mosabwezeza. 12Ndipo Yehova anaonekera kwa Solomo usiku,
nanena naye, Ndamva pemphero lako, ndadzisankhira malo ano
akhale nyumba ya nsembe. 13Ndikatseka kumwamba kuti
pasakhale mvula, kapena ndikalamulira dzombe lithe za padziko,
kapena ndikatumiza mliri mwa anthu anga; 14ndipo anthu anga

ochedwa dzina langa akadzicepetsa, nakapemphera, nakafuna nkhope yanga, nakatembenuka kuleka njira zao zoipa; pamenepo ndidzamvera m'Mwamba, ndi kukhululukira coipa cao, ndi kuciritsa dziko lao. 15Tsopano maso anga adzakhala otsegukira, ndi makutu anga ochera, pemphero la m'malo ano. 16Pakuti ndasankha ndi kuipatula nyumba Iyi, kuti dzina langa likhaleko cikhalire; inde maso anga ndi mtima wanga zidzakhala komweko kosalekeza. 17Ndipo iwe ukadzayenda pamaso panga monga umo anayendera Davide atate wako, nukacita monga mwa zonse ndakulamulira iwe, nukasunga malemba anga ndi maweruzo anga; 18pamenepo ndidzakhazikitsa mpando wacifumu wa ufumu wako, monga ndinapangana ndi Davide atate wako, ndi kuti, Sadzakusowa munthu wokhala mfumu m'Israyeli. 19Koma mukabwerera inu, ndi kusiya malemba anga, ndi malamulo anga, amene ndaika pamaso panu, ndi kumuka ndi kutumikira milungu yina ndi kuilambira; 20pamenepo ndidzawazula m'dziko langa limene ndinawapatsa; ndi nyumba yino ndinaipatulira dzina langa ndidzaitaya, osaionanso, ndi kuiyesa mwambi ndi mnyozo mwa mitundu yonse ya anthu. 21Ndi munthu yense wakupita pa nyumba iyi yaitali adzadabwa nayo, nadzati, Yeliova ana tero ndi dziko lino ndi nyumba yino cifukwa ninji? 22Ndipo adzayankha, Popeza anasiya Yehova Mulungu wa makolo ao amene anawaturutsa m'dziko la Aigupto, nagwira milungu yina, nailambira ndi kuitumikira; cifukwa cace anawagwetsera coipa ici conse.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Solomo amanga midzi yina

1Ndipo kunali, zitatha zaka makumi awiri m'mene anamanga
nyumba ya Yehova, ndi nyumba yace yace, 2Solomo anamanga
midzi imene Huramu adampatsa, nakhalitsamo ana a Israyeli.
3Ndipo Solomo anamuka ku Hamati Zoba, naugonjetsa. 4Ndipo
anamanga Tadimori m'cipululu, ndi midzi yonse yosungiramo
cuma, imene anaimanga m'Hamati. 5Anamanganso Betihoroni wa
kumtunda, ndi Betihoroni wa kunsi, midzi ya malinga yokhala nao
malinga, zitseko, ndi mipiringidzo; 6ndi Balati, ndi midzi yonse
yosungiramo cuma anali nayo Solomo, ndi midzi yonse ya
magareta ace, ndi midzi ya apakavalo ace, ndi zonse anazifuna
Solomo kuzimanga zomkondweretsa m'Yerusalemu, ndi m'Lebano,
ndi m'dziko lonse la ufumu wace. 7Ndipo anthu onse otsala mwa
Ahiti, ndi Aamori, ndi Aperizi, ndi Ahivi, ndi Ayebusi, osati
Aisrayeli, 8mwa ana ao otsala m'dziko pambuyo pao, amene ana a
Israyeli sanawatha, mwa iwowa Solomo anawacititsa thangata
mpaka lero lino. 9Koma mwa ana a Israyeli Solomo sanawayesa
akapolo omgwirira nchito; koma iwowa anali anthu a nkhondo,
akazembe ace akuru, ndi akuru a magareta ace, ndi apakavalo
ace. 10Amenewa anali akuru a akapitao a mfumu Solomo, ndiwo
mazana awiri mphambu makumi asanu akulamulira anthu. 11Ndipo
Solomo anamkweretsa mwana wamkazi wa Farao m'mudzi wa
Davide, alowe m'nyumba imene adammangira; pakuti anati, Mkazi
wanga asakhale m'nyumba ya Davide mfumu ya Israyeli; popeza
mpopatulika pamene panafika likasa la Yehova.

Malongosoledwe a cipembedzo ndi nsembezo

12Pamenepo Solomo anapereka nsembe zopsereza kwa Yehova pa
guwa la nsembe la Yehova, limene adalimanga pakhomo
palikole, 13monga momwe mudayenera, tsiku ndi tsiku; napereka
monga momwe adauza Mose pamasabata, pokhala mwezi, ndi pa
madyerero oikika, katatu m'caka, pa madyerero ali mkate
wopanda cotupitsa, ndi pa madyerero a masabata, ndi pa
madyerero a misasa. 14Ndipo anaika monga mwa ciweruzo ca
Davide atate wace zigawo za ansembe ku utumiki wao, ndi Alevi
ku udikiro wao, kulemekeza Mulungu, ndi kutumikira pamaso pa
ansembe, monga munayenera tsiku ndi tsiku; odikira omwe monga
mwa zigawo zao ku cipata ciri conse; pakuti momwemo Davide
munthu wa Mulungu adamuuza. 15Ndipo sanapambuka pa lamulo
la mfumu la kwa ansembe ndi Alevi, kunena za kanthu kali konse,
kapena za cumaci. 16Momwemo nchito yonse ya Solomo
inakonzekeratu tsiku lakuika maziko a nyumba ya Yehova, mpaka
anaitsiriza. 17Pamenepo Solomo anamuka ku Ezioni Geberi, ndi ku
Eloti pambali pa nyanja, m'dziko la Edomu. 18Ndipo Huramu

anamtumizira zombo, ndi amarinyero ace, ndi anyamata akudziwa za m'nyanja; ndipo anamuka pamodzi ndi anyamata a Solomo ku Ofiri, natengako matalente mazana anai mphambu makumi asanu a golidi, nabwera nao kwa Solomo mfumu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Mfumu yaikazi ya ku Seba aceza ndi Solomo

1Ndipo atamva mfumu yaikazi ya ku Seba mbiri ya Solomo, anadza
kumuyesera Solomo ndi miyambi yododometsa ku Yerusalemu, ndi ulendo
waukuru, ndi ngamila zosenza zonunkhira, ndi golidi wocuruka, ndi timiyala ta
mtengo wace; ndipo atafika kwa Solomo anakamba naye zonse za m'mtima
mwace. 2Ndipo Solomo anammasulira mau ace onse, panalibe kanthu
kombisikira Solomo, kamene sanammasulira. 3Ndipo mfumu yaikazi ya ku
Seba ataiona nzeru ya Solomo, ndi nyumba adaimanga, 4ndi zakudya za pa
gome lace, ndi makhalidwe a anyamata ace, ndi maimiriridwe a atumiki ace,
ndi mabvalidwe ao, ndi otenga zikho ace, ndi mabvalidwe ao, ndi
makweredwe ace pokwera iye kumka ku nyumba ya Yehova, munalibenso
moyo mwa iye. 5Ndipo anati kwa mfumu, Inali yoona mbiri ija ndidaimva
m'dziko langa, ya macitidwe anu, ndi ya nzeru zanu. 6Koma sindinakhulupira
mau ao mpaka ndinadza, ndaona ndi maso anga; ndipo taonani
anandifotokozera dera lina lokha la nzeru zanu zocuruka; mwa, onjezatu pa
mbiri ndidaimva. 7Odala anthu anu, ndi odala anyamata anu awa akuima
ciimirire pamaso panu, ndi kumva nzeru zanu. 8Wolemekezeka Yehova
Mulungu wanu, wakukondwera nanu, kukuikani pa mpando wacifumu wace,
mukhalire Yehova Mulungu wanu mfumu pa anthu ace; popeza Mulungu wanu
anakonda Aisrayeli kuwakhazika kosatha, anakulongani mfumu yao, kucita
ciweruzo ndi cilungamo. 9Ndipo mkaziyo anapatsa mfumu matalente a golidi
zana limodzi mphambu makumi awiri, ndi zonunkhira zambiri ndithu, ndi
timiyala ta mtengo wace; panalibe zonunkhira zina zonga zija mfumu yaikazi
ya ku Seba anapatsa mfumu Solomo. 10Ndiponso anyamata a Huramu, ndi
anyamata a Solomo otenga golidi ku Ofiri, anatenga mitengo yambawa ndi
timiyala ta mtengo wapatali. 11Ndipo mfumu inasema mitengo yambawa
ikhale mizati ya nyumba ya Yehova, ndi nyumba ya mfumu, ndi azeze, ndi
zisakasa za oyimbira; sizinaoneka zotere ndi kale lonse m'dziko la
Yuda. 12Ndipo mfumu Solomo anampatsa mfumu yaikazi ya ku Seba cifuniro
cace conse, ciri conse anacipempha, osawerengera zija adabwera nazo kwa
mfumu. Momwemo anabwerera, namuka ku dziko lace, iyeyu ndi anyamata
ace.

Cuma ndi ulemerero wa Solomo

13Kulemera kwace tsono kwa golidi anafika kwa Solomo caka cimodzi ndiko
matalente mazana asanu ndi limodzi mphambu makumi asanu ndi limodzi
kudza asanu ndi limodzi a golidi; 14osawerenga uja anabwera naye amalonda
oyendayenda, ndi amalonda ena; ndipo mafumu onse a Arabiya, ndi
akazembe a dziko, anadza naye golidi ndi siliva kwa Solomo. 15Ndipo mfumu
Solomo anapanga zikopa mazana awiri za golidi wonsansantha, cikopa
cimodzi cinathera golidi wonsansantha masekeli mazana awiri. 16Napanganso
malihawo mazana atatu a golidi wonsansantha, cikopa cimodzi cinathera
masekeli mazana atatu a golidi; ndipo mfumu inazilonga m'nyumba yochedwa
Nkhalango ya Lebano. 17Mfumu inapanganso mpando wacifumu waukuru wa
minyanga, naukuta ndi golidi woona. 18Ndi mpando wacifumuwo unali nao
makwerero asanu ndi limodzi, ndi copondapo mapazi cagolidi, omangika ku
mpandowo; ndi ku mbali zonse ziwiri za pokhalirapo kunali manja; ndi
mikango iwiri inaimirira m'mbali mwa manjawo. 19Ndi mikango khumi ndi iwiri
Inaimirirapo, mbali yina ndi yina, pa makwerero asanu ndi limodzi;
sanapangidwa wotere m'ufumu uli wonse. 20Ndipo zikho zomwera zonse za
Solomo zinali zagolidi, ndi zipangizo zonse za nyumba yochedwa Nkhalango
ya Lebano zinali za golidi woona; siliva sanayesedwa kanthu m'masiku a

Solomo. 21Pakuti zombo za mfumu zinayenda ku Tarisi ndi anyamata a
Huramu; zombo za ku Tarisi zinadza kamodzi zitapita zaka zitatu, ndi kubwera
nazo golidi, ndi siliva, minyanga, ndi apusi, ndi mbalame za zitsukwa zazitali
za mawanga mawanga. 22Mamwemo mfumu Solomo inaposa mafumu onse a
pa dziko lapansi, kunena za cuma ndi nzeru. 23Ndipo mafumu onse a pa dziko
lapansi anafuna nkhope ya Solomo, kudzamva nzeru zace Mulungu adazilonga
m'mtima mwace. 24Nabwera nao munthu yense mtulo wace, zipangizo
zasiliva, ndi zipangizo zagolidi, zobvala, ndi zobvala za nkhondo, ndi
zonunkhira, akavalo, ndi nyuru; momwemo caka ndi caka. 25Ndipo Solomo
anali nazo zipinda zikwi zinai za akavalo ndi magareta, ndi apakavalo zikwi
khumi ndi ziwiri; nawaika m'toidzi ya magareta, ndi m'Yerusalemu kwa
mfumu. 26Ndipo analamulira mafumu onse kuyambira ku Firate kufikira ku
dziko la Afilisti, ndi ku malire a ku Aigupto. 27Ndipo mfumu inacurukitsa siliva
m'Yerusalemu ngati miyala; ndi mikungudza anailinganiza ndi mikuyu iri
kumadambo kucuruka kwace. 28Ndipo anakamtengera Solomo akavalo ku
Aigupto, ndi ku maiko onse.

Kumwalira kwa Solomo

29Macitidwe ena tsono a Solomo, oyamba ndi otsiriza, salembedwa kodi
m'buku la mau a Natani mneneri ndi m'zonenera za Ahiya wa ku Silo, ndi
m'masomphenya a Ido mlauli za Yerobiamu mwana wa Nebati? 30Ndipo
Solomo anakhala mfumu ya Israyeli yense m'Yerusalemu zaka makumi
anai. 31Nagona Solomo pamodzi ndi makolo ace, naikidwa m'mudzi wa
Davide atate wace; ndipo Rehabiamu mwana wace anakhala mfumu m'malo
mwace.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Ufumu ugawanika pakati. Rehabiamu mfumu ya Yuda, Yerobiamu ya Israyeli

1Ndipo Rehabiamu anamuka ku Sekemu; pakuti Aisrayeli onse
adadza ku Sekemu kumlonga ufumu. 2Ndipo kunali, atamva
Yerobiamu mwana wa Nebati (popeza anali m'Aigupto kumene
adathawira, kuthawa Solomo mfumu), Yerobiamu anabwera kucoka
ku Aigupto. 3Ndipo anatuma munthu kukamuitana, nadza
Yerobiamu ndi Aisrayeli onse, nalankhula ndi Rehabiamu, ndi
kuti, 4Atate wanu analemeretsa goli lathu; inu tsono pepuzaniko
nchito yolemetsa ya atate wanu, ndi goli lace lolemera
anatisenzetsali, ndipo tidzakutumikirani. 5Ndipo ananena nao,
Mubwerenso atapita masiku atatu. Nacoka anthu. 6Ndipo
Rehabiamu mfumu anafunsana ndi akulu akulu, amene anaimirira
pamaso pa Solomo atate wace akali ndi moyo, nati, Mundipangire
bwanji, kuti ndiwabwezere mau anthu awa? 7Ndipo ananena naye,
kuti, Mukawacitira cokoma anthu awa, ndi kuwakonda, ndi
kulankhula nao mau okoma, adzakhala anyamata anu
kosatha. 8Koma analeka uphungu wa akulu akuluwa
adampangirawo, nakafunsana ndi anyamata anakula naye
pamodzi, oimirira pamaso pace. 9Nati nao, Mundipangire bwanji
inu, kuti tibwezere mau anthu awa ananena nanewo, ndi kuti,
Mupepuze goli limene atate wanu anatisenzetsa ife? 10Ndipo
anyamatawo adakula naye pamodzi ananena naye, ndi kuti,
Muzitero nao anthu awa adalankhula nanu, ndi kuti, Atate wanu
analemeretsa goli lathu, koma inu mutipepuzire ilo; muzitero nao,
Kanense wanga adzaposa m'cuuno mwa atate wanga. 11Ndipo
tsopano, popeza atate wanga anakusenzetsani goli lolemera, ine
ndidzaonjezerapo pa goli lanu; atate wanga anakukwapulani ndi
zikoti, koma ine ndidzakukwapulani ndi zinkhanira. 12Tsono
Yerobiamu ndi anthu onse anabwera kwa Rehabiamu tsiku lacitatu,
monga mfumu idanena, ndi kuti, Bweraninso kwa ine tsiku
lacitatu. 13Ndipo mfumu inawayankha mokaripa, popeza mfumu
Rehabiamu analeka uphungu wa akulu akulu, 14nalankhula nao
monga umo anampangira acinyamata, ndi kuti, Atate wanga
analemeretsa goli lanu, koma ine ndidzaonjezerapo; atate wanga
anakukwapulani ndi zikoti, koma ine ndidzakukwapulani ndi
zinkhanira. 15Momwemo mfumu siinamvera anthuwo; pakuti
kusinthaku kudafuma kwa Mulungu, kuti Yehova akhazikitse mau
ace, amene ananenetsa Ahiya wa ku Silo kwa Yerobiamu mwana
wa Nebati. 16Ndipo pakuona Aisrayeli onse kuti mfumu
sinawamvera anthuwo, anamyankha mfumu, ndi kuti, Tiri naye
ciani Davide? inde tiribe colowa m'mwana wa Jese; tiyeni kwathu,
Aisrayeli inu; yang'anira nyumba yako tsopano, Davide. Momwemo

Aisrayeli onse anamuka ku mahema ao. 17Koma za ana a Israyeli
okhala m'midzi ya Yuda, Rehabiamu anakhalabe mfumu
yao. 18Pamenepo Rehabiamu mfumu inatuma Hadoramu
woyang'anira thangata; koma ana a Israyeli anamponya miyala,
nafa. Ndipo Rehabiamu mfumu anafulumira kukwera pa gareta
wace kuthawira ku Yerusalemu. 19Motero Israyeli anapandukana
nayo nyumba ya Yuda mpaka lero lino.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Mulungu aletsa nkhondo pakati pa Yuda ndi Israyeli

1Ndipo atafika ku Yerusalemu Rehabiamu, anamemeza a nyumba
ya Yuda ndi Benjamini amuna osankhika zikwi zana limodzi
mphambu makumi asanu ndi atatu, ndiwo ankhondo, alimbane ndi
Aisrayeli kubwezanso ufumu kwa Rehabiamu. 2Koma mau a Yehova
anadza kwa Semaya munthu wa Mulunguyo, ndi kuti, 3Lankhula
ndi Rehabiamu mwana wa Solomo mfumu ya Yuda ndi Benjamini,
ndi kuti, 4Atero Yehova, Musamuka kukayambana ndi abale anu,
bwererani yense ku nyumba yace; pakuti cinthu ici cifuma kwa Ine.
Ndipo anamvera mau a Yehova, nabwerera osakayambana ndi
Yerobiamu. 5Ndipo Rehabiamu anakhala m'Yerusalemu, namanga
midzi yolimbikiramo m'Yuda. 6Anamangadi Betelehemu, ndi
Etamu, ndi Tekoa, 7ndi Betezuri, ndi Soko, ndi Adulamu, 8ndi Gati,
ndi Maresa, ndi Zifi, 9ndi Adoraimu, ndi Lakisi, ndi Azeka, 10ndi
Zora, ndi Ayaloni, ndi Hebroni; ndiyo midzi yamalinga ya m'Yuda
ndi Benjamini. 11Ndipo analimbitsa malingawo, naikamo atsogoleri,
ndi cakudya cosungikiratu, ndi mafuta, ndi lvinyo. 12Ndi m'midzi iri
yonse anaikamo zikopa ndi mikondo, nailimbitsa cilimbitsire. Ndipo
Yuda ndi Benjamini anakhala ace.

Alevi ndi Aisrayeli ambiri afika ku Yerusalemu

13Ndipo ansembe ndi Alevi okhala m'Israyeli lonse anadziphatikiza
kwa iye, ocokera m'malire ao Onse. 14Pakuti Alevi anasiya
podyetsa pao, ndi maiko ao ao, nadza ku Yuda ndi ku Yerusalemu;
popeza Yerobiamu ndi ana ace anawataya, kuti asacitire Yehova
nchito ya nsembe; 15nadziikira ansembe a misanje, ndi a ziwanda,
ndi a ana a ng'ombe adawapanga. 16Ndipo akuwatsata iwo anadza
ku Yerusalemu, ocokera m'mafuko onse a Israyeli, iwo akupereka
mitima yao kufuna Yehova Mulungu wa Israyeli, kudzaphera
Yehova Mulungu wa makolo ao nsembe. 17Momwemo analimbikitsa
ufumu wa Yuda, nalimbikitsa Rehabiamu, mwana wa Solomo zaka
zitatu; pakuti anayenda m'njira ya Davide ndi Solomo zaka
zitatu. 18Ndipo Rehabiamu anadzitengera mkazi Mahalati, mwana
wamkazi wa Yerimoti mwana wa Davide, ndi wa Abihaili mwana
wamkazi wa Eliabu mwana wa Jese; 19ndipo anambalira ana, Yeusi,
ndi Semariya, ndi Zahamu. 20Ndi pambuyo pace anatenga Maaka
mwana wamkazi wa Abisalomu; ndipo anambalira Abiya, ndi Atai,
ndi Ziza, ndi Selomiti. 21Ndipo Rehabiamu anakonda Maaka mwana
wamkazi wa Abisalomu koposa akazi ace onse, ndi akazi ace
ang'ono (pakuti adatenga akazi khumi mphambu asanu ndi atatu,
ndi akazi ang'ono makumi asanu ndi limodzi, nabala ana amuna
makumi awiri mphambu asanu ndi atatu, ndi ana akazi makumi
asanu ndi limodzi). 22Ndipo Rehabiamu anaika Abiya mwana wa

Maaka akhale wamkuru, kalonga mwa abale ace; ndiko kuti adzamlonga ufumu.
23Ndipo anacita mwanzeru, nabalalitsa ana ace amuna onse m'maiko onse a Yuda ndi Benjamini, ku midzi yonse yamalinga; nawapatsa cakudya cocuruka, nawafunira akazi ocuruka.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Sisaki wa ku Aigupto athira nkhondo Rehabiamu

1Ndipo kunacitika, utakhazikika ufumu wa Rehabiamu, nalimbika
iye, anasiya cilamulo ca Yehova, ndi Aisrayeli onse pamodzi
naye. 2Ndipo Rehabiamu atakhala mfumu zaka zinai, Sisaki mfumu
ya ku Aigupto anakwerera Yerusalemu, popeza iwo adalakwira
Yehova. 3Anakwera ndi magareta cikwi cimodzi mphambu mazana
awiri, ndi apakavalo zikwi makumi asanu ndi limodzi, ndi anthu
adadza naye kuturuka m'Aigupto ngosawerengeka, Alubi, Asuki,
ndi Akusi. 4Ndipo analanda midzi yamalinga yokhala ya Yuda,
nadza ku Yerusalemu. 5Pamenepo Semaya mneneri anadza kwa
Rehabiamu, ndi kwa akalonga a Yuda, atasonkhana ku Yerusalemu
cifukwa ca Sisaki, nati nao, Atero Yehova, Inu mwandisiya Ine,
cifukwa cace Inenso ndasiya inu m'dzanja la Sisaki. 6Pamenepo
akalonga a Israyeli ndi mfumu anadzicepetsa, nati, Yehova ali
wolungama. 7Ndipo pamene Yehova anaona kuti anadzicepetsa,
mau a Yehova anadza kwa Semaya, ndi kuti, Anadzicepetsa;
sindidzawaononga; koma katsala kanthawi ndipo ndidzawapatsa
cipulumutso, wosatsanulira mkwiyo wanga pa Yerusalemu ndi
dzanja la Sisaki. 8Koma adzakhala akapolo ace, kuti adziwe
kunditumikira kwanga, ndi kuwatumikira kwa maufumu a maiko.

Sisaki alanda cuma ca Kacisi ndi ca nyumba ya mfumu

9Ndipo Sisaki mfumu ya Aigupto anakwerera Yerusalemu, nacotsa
cuma ca m'nyumba ya Yehova, ndi cuma ca m'nyumba ya mfumu;
anazicotsa zonse; anacotsanso zikopa zagolidi adazipanga
Solomo. 10Ndipo Rehabiamu mfumu anapanga m'malo mwa izo
zikopa zamkuwa, nazipereka m'manja mwa kapitao wa olindirira
akusunga pakhomo pa nyumba ya mfumu. 11Ndipo kunatero kuti
pakulowa mfumu m'nyumba ya Yehova, anadza olindirira,
nazinyamula, nazibwezanso ku cipinda ca olindirira. 12Ndipo
pakudzicepetsa iye mkwiyo wa Mulungu unamcokera, kuti
usamuononge konse; ndiponso munatsalira zokoma
m'Yuda. 13Nadzilimbitsa Rehabiamu mfumu m'Yerusalemu, nacita
ufumu; pakuti Rehabiamu anali wa zaka makumi anai mphambu
cimodzi polowa ufumu wace, nakhala mfumu zaka khumi ndi
zisanu ndi ziwiri m'Yerusalemu, ndiwo mudzi Yehova adausankha
m'mafuko onse a Israyeli, kuikapo dzina lace; ndipo dzina la mace
ndiye Naama M-amoni. 14Koma anacita coipa, popeza
sanalunjikitsa mtima wace kufuna Yehova. 15Macitidwe ace tsono a
Rehabiamu, zoyamba ndi zotsiriza, sizilembedwa kodi m'buku la
mau a Semaya mneneriyo, ndi la Ido mlauliyo, lakunena za
zibadwidwe? Ndipo panali nkhondo pakati pa Rehabiamu ndi
Yerobiamu masiku onse. 16Nagona Rehabiamu ndi makolo ace,

naikidwa m'mudzi wa Davide; ndipo Abiya mwana wace anakhala mfumu m'malo mwace.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Abiya ndi Yerobiamu agwirana nkhondo, Israyeli akanthidwa

1Ndipo caka cakhumi mphambu zisanu ndi zitatu ca Yerobiamu,
Abiya analowa ufumu wa Yuda. 2Anakhala mfumu m'Yerusalemu
zaka zitatu; ndi dzina la mace ndiye Mikaya mwana wamkazi wa
Uriyeli wa ku Gibeya. Ndipo panali nkhondo pakati pa Abiya ndi
Yerobiamu. 3Ndipo Abiya anayambana nkhondo ali ndi khamu la
ngwazi za nkhondo, amuna osankhika zikwi mazana anai;
Yerobiamu atandandalitsa nkhondo yace ilimbane naye ndi amuna
osankhika zikwi mazana asanu ndi atatu, ndiwo ngwazi
zamphamvu. 4Ndipo Abiya anaimirira pa phiri la Zemaraimu, ndilo
ku mapiri a Efraimu, nati, Mundimvere Yerobiamu ndi Aisrayeli
onse; 5simudziwa kodi kuti Yehova Mulungu wa Israyeli anapereka
ciperekere ufumu wa Israyeli kwa Davide, kwa iye ndi ana ace, ndi
pangano la mcere? 6Koma Yerobiamu mwana wa Nebati mnyamata
wa Solomo mwana wa Davide anauka, napandukana ndi mbuye
wace. 7Ndipo anamsonkhanira amuna acabe, anthu opanda pace,
ndiwo anadzilimbikitsa kutsutsana naye Rehabiamu mwana wa
Solomo, muja Rehabiamu anali mnyamata ndi woolowa mtima,
wosakhoza kuwalaka. 8Ndipo tsopano, mukuti mudzilimbikitse
kutsutsana nao ufumu wa Yehova m'dzanja la ana a Davide; ndinu
aunyinji ambiri, ndi pamodzi nanu ana a ng'ombe agolidi
adawapanga Yerobiamu akhale milungu yanu. 9Simunapitikitsa
kodi ansembe a Yehova, ana a Aroni, ndi Alevi, ndi kudziikira
ansembe monga amacita anthu a m'maiko ena? kuti ali yense
wakudza kudzipatulira ndi mwana wa ng'ombe, ndi nkhosa
zamphongo zisanu ndi ziwiri, yemweyo ndiye wansembe wa iyo
yosati milungu. 10Koma ife, Yehova ndiye Mulungu wathu,
sitinamsiya Iye; ndi ansembe tiri nao akutumikira Yehova ana a
Aroni, ndi. Alevi, m'nchito mwao, 11nafukizira Yehova nsembe
zopsereza m'mawa ndi m'mawa, ndi madzulo onse, ndi zonunkhira
za pfungo lokoma, nakonza mkate woonekera pa gome lopatulika,
ndi coikapo nyali cagolidi ndi nyali zace, ziyake madzulo onse;
pakuti tisunga cilangizo ca Yehova Mulungu wathu, koma inu
mwamsiya Iye. 12Ndipo taonani, Mulungu ali nafe, wotitsogolera
ndi ansembe ace, ndi malipenga oliza nao cokweza, kukulizirani
inu cokweza. Ana a Israyeli inu, musalimbane naye Yehova
Mulungu wa makolo anu; pakuti simudzapindula nako. 13Koma
Yerobiamu anazunguliritsa owalalira, awadzere kumbuyo;
momwemo iwowa anali kumaso kwa Yuda, ndi owalalira anali
kumbuyo kwao. 14Ndipo poceuka Yuda, taonani, nkhondo
inayambana nao kumaso ndi kumbuyo; napfuulira iwo kwa Yehova,
ndi ansembe analiza malipenga. 15Pamenepo amuna a Yuda
anapfuula cokweza; ndipo popfuula amuna a Yuda, kunacitika kuti

Mulungu anakantha Yerobiamu ndi Aisrayeli onse pamaso pa Abiya
ndi Yuda. 16Ndipo ana a Israyeli anathawa pamaso pa Yuda,
nawapereka Mulungu m'dzanja lao. 17Ndipo Abiya ndi anthu ace
anawakantha makanthidwe akuru; nagwa, nafa amuna osankhika
zikwi mazanaasanu a Israyeli. 18Momwemo anacepetsedwa ana a
Israyeli nthawi ija, nalakika ana a Yuda; popeza anatama Yehova
Mulungu wa makolo ao. 19Ndipo Abiya analondola Yerobiamu,
namlanda midzi yace, Beteli ndi miraga yace, ndi Yesana ndi
miraga yace, ndi Efroni ndi miraga yace. 20Ndi Yerobiamu
sanaonanso mphamvu m'masiku a Abiya, namkantha Yehova, wa
iye. 21Koma Abiya anakula mphamvu, nadzitengera akazi khumi
ndi anai, nabala ana amuna makumi awiri mphambu awiri, ndi ana
akazi khumi mphambu asanu ndi mmodzi. 22Macitidwe ena tsono a
Abiya, ndi mayendedwe ace, ndi mau ace, alembedwa m'buku
lomasulira la mneneri Ido.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Asa akantha Akusi

1Momwemo Abiya anagona ndi makolo ace, ndipo anamuika
m'mudzi wa Davide; ndi Asa mwana wace anakhala mfumu
m'malo mwace, m'masiku ace dziko linaona bata zaka
khumi. 2Ndipo Asa anacita cokoma ndi coyenera m'maso mwa
Yehova Mulungu wace, 3nacotsa maguwa a nsembe acilendo, ndi
misanje; naphwanya zoimiritsa zao, nalikha zifanizo zao, 4nauza
Yuda afune Yehova Mulungu wa makolo ao, ndi kucita cilamulo ndi
cowauza, Iye. 5Anacotsanso m'midzi yonse ya Yuda misanje, ndi
zifanizo za dzuwa; ndi ufumuwo unacita bata pamaso pace. 6Ndipo
anamanga midzi yamalinga m'Yuda; pakuti dziko linacita bata,
analibe nkhondo iyeyu zaka zija, popeza Yehova
anampumulitsa. 7Ndipo anati kwa Yuda, Timange midzi iyi ndi
kuizingira malinga, ndi nsanja, zitseko, ndi mipiringidzo; dziko likali
pamaso pathu, popeza tafuna Yehova Mulungu wathu; tamfuna
Iye, natipatsa mpumulo pozungulira ponse. Momwemo anamanga
mosabvutika. 8Ndipo Asa anali nao ankhondo ogwira zikopa ndi
mikondo, a m'Yuda zikwi mazana atatu; ndi a m'Benjamini ogwira
malihawo ndi okoka mauta zikwi mazana awiri mphambu makumi
asanu ndi atatu; onsewo ngwazi zamphamvu. 9Ndipo
anawaturukira Zera Mkusi ndi ankhondo zikwi cikwi cimodzi, ndi
magareta mazana atatu; nafika iye ku Maresa. 10Naturuka Asa
pamaso pace, nanika nkhondoyi m'cigwa ca Sefata ku
Maresa. 11Ndipo Asa anapfuulira kwa Yehova Mulungu wace, nati,
Yehova, palibe wina ngati Inu, kuthandiza pakati pa wamphamvu
ndi iye wopanda mphamvu; tithandizeni Yehova Mulungu wathu,
titama Inu, taturukira aunyinji awa m'dzina lanu. Yehova, Inu ndinu
Mulungu wathu, munthu asakulakeni. 12Ndipo Yehova anakantha
Akusi pamaso pa Asa ndi Yuda, nathawa Akusi. 13Ndi Asa ndi anthu
anali naye anawalondola mpaka ku Gerari, nagwa Akusi ambiri
osalimbikanso mphamvu iwowa; pakuti anathyoledwa pamaso pa
Yehova ndi ankhondo ace; ndipo anatenga zofunkha
zambiri. 14Ndipo anakantha midzi yonse pozungulira pace pa
Gerari; a pakuti mantha ocokera kwa Yehova anawagwera; ndipo
anafunkha m'midzi monse, pakuti mudacuruka zofunkha
m'menemo. 15Anakanthanso a m'mahema a ng'ombe, nalanda
nkhosa zocuruka, ndi ngamila; nabwerera kumka ku Yerusalemu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Asa acotsa mafano nabwereza cipangano ndi Mulungu

1Pamenepo mzimu wa Mulungu unagwera Azariya mwana wa
Odedi, 2ndipo anaturuka kukomana naye Asa, nanena naye,
Mundimvere, Asa, ndi onse Ayuda ndi Abenjamini, Yehova ali nanu;
mukakhala ndi Iye, mukamfuna Iye, mudzampeza; koma
mukamsiya, adzakusiyani. 3Masiku ambiri tsono Israyeli anakhala
wopanda Mulungu woonayo, ndi wopanda wansembe
wakuphunzitsa, ndi wopanda cilamulo; 4koma pamene
anatembenukira kwa Yehova Mulungu wa Israyeli m'kusautsidwa
kwao, ndi kumfuna, anampeza. 5Ndipo nthawi zija panalibe
mtendere kwa iye wakuturuka, kapena kwa iye wakulowa, koma
mabvuto akuru anagwera onse okhala m'maikomo. 6Ndipo
anapasulidwa, mtundu wa anthu kupasula unzace, ndi mudzi
kupasula mudzi; pakuti Mulungu anawabvuta ndi masautso ali
onse. 7Koma limbikani inu, manja anu asalende; pakuti ku nchito
yanu kuli mphotho. 8Ndipo pakumva Asa mau awa, ndi cinenero ca
Odedi mneneriyo, analimbika mtima, nacotsa zonyansazo m'dziko
lonse la Yuda ndi Benjamini, ndi m'midzi adailanda ku mapiri a
Efraimu; nakonza guwa la nsembe la Yehova lokhala pakhomo pa
likole la Yehova. 9Namemezaonse a m'Yuda ndi m'Benjamini, ndi
iwo akukhala nao ocokera ku Efraimu, ndi Manase, ndi Simeoni;
pakuti anamdzera ocuruka ocokera ku Israyeli, pamene anaona
kuti Yehova Mulungu wace anali naye. 10Ndipo anasonkhana ku
Yerusalemu mwezi wacitatu, Asa atakhala mfumu zaka khumi ndi
zinai. 11Naphera Yehova nsembe tsiku lija za zofunkha adabwera
nazo, ng'ombe mazana asanu ndi awiri, ndi nkhosa zikwi zisanu ndi
ziwiri. 12Nalowa cipangano cakufuna Yehova Mulungu wa makolo
ao ndi mtima wao wonse, ndi moyo wao wonse; 13ndi kuti yense
wosafuna Yehova Mulungu wa Israyeli aphedwe, ngakhale
wamng'ono kapena wamkuru, wamwamuna kapena
wamkazi. 14Ndipo analumbira kwa Yehova ndi mau akuru, ndi
kupfuula ndi mphalasa ndi malipenga. 15Ndipo Yuda yense
anakondwera nalo lumbirolo; pakuti adalumbira ndi mtima wao
wonse, namfunafuna ndi cifuno cao conse; ndipo anampeza; ndi
Yehova anawapumulitsa pozungulirapo. 16Maaka yemwe, mai wace
wa Asa, mfumu, anamcotsa uyu asakhalenso mai wa ufumu,
popeza anapanga fano loopsa la Asera; ndipo Asa analikha fano
lace, naliphwanyaphwanya, nalitenthera ku mtsinje wa
Kedroni. 17Cinkana misanje siinacotsedwa m'Israyeli, mtima wa
Asa unali wangwiro masiku ace onse. 18Ndipo analowa nazo
zopatulika za atate wace, ndi zopatulika zace zace, ku nyumba ya
Mulungu; ndizo siliva, ndi golidi, ndi zipangizo. 19Ndipo panalibenso

nkhondo mpaka Asa atakhala mfumu zaka makumi atatu mphambu zinai.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Asa apangana ndi Benihadadi, nalimbana ndi Israyeli

1Caka ca makumi atatu mphambu zisanu ndi cimodzi ca Asa, Basa
mfumu ya Israyeli anakwera kulimbana ndi Yuda, namangitsa
Rama, kuwaletsa anthu asaturuke kapena kulowa kwa Asa mfumu
ya Yuda. 2Pamenepo Asa anaturutsa siliva ndi golidi ku cuma ca
nyumba ya Yehova, ndi ca nyumba ya mfumu; nazitumiza kwa
Benihadadi mfumu ya Aramu, yokhala ku Damasiko, ndi
kuti, 3Pakhale pangano pakati pa ine ndi inu, monga pakati pa
atate wange ndi atate wanu; taonani, ndakutumizirani siliva ndi
golidi; mukani, pasulani pangano lanu ndi Basa mfumu ya Israyeli,
kuti andicokere. 4Ndipo Benihadadi anamvera mfumu Asa
natumiza akazembe a magulu ace a nkhondo ayambane ndi midzi
ya Israyeli, nakantha Iyoni, ndi Dani, ndi Abelimaimu, ndi midzi
yonse ya cuma ya Nafitali, 5Ndipo kunali, pakumva ici Basa,
analeka kumangitsa Rama, naleketsa nchito yace. 6Pamenepo Asa
mfumu anatenga Ayuda onse, ndipo anatuta miyala ya ku Rama,
ndi mitengo yace, imene Basa adamanga nayo, namangira Geba
ndi Mizipa.

Hanani mlauli adzudzula Asa

7Nthawi yomweyi Hanani mlauli anadza kwa Asa mfumu ya Yuda,
nanena naye, Popeza mwatama mfumu ya Aramu, osatama
Yehova Mulungu wanu, cifukwa cace khamu la nkhondo la mfumu
ya Aramu lapulumuka m'dzanja lanu. 8Nanga Akusi ndi Alubi,
sanakhala khamu lalikurukuru, ndi magareta ndi apakavalo
ambirimbiri, koma muja munatama Yehova anawapereka m'dzanja
mwanu? 9Pakuti maso a Yehova ayang'ana uko ndi uko m'dziko
lonse lapansi, kudzionetsera wamphamvu kwa iwo amene mtima
wao uli wangwiro ndi Iye. Mwacita copusa m'menemo; pakuti
kuyambira tsopano mudzaona nkhondo. 10Koma Asa anakwiya
naye mlauliyo, namuika m'kaidi; pakuti adapsa mtima naye
cifukwa ca ici. Nthawi yomweyi Asa anasautsa anthu ena. 11Ndipo
taonani, zocita Asa, zoyamba ndi zotsiriza, zalembedwa m'buku la
mafumu a Yuda ndi Israyeli. 12Ndipo Asa atakhala mfumu zaka
makumi atatu mpham bu zisanu ndi zitatu, anadwala nthenda ya
mapazi, nikuladi nthendayi; koma podwala iye sanafuna Yehova,
koma asing'anga. 13Nagona Asa ndi makolo ace, namwalira
atakhala mfumu zaka makumi anai. 14Ndipo anamuika m'manda
ace adadzisemerawo m'mudzi wa Davide, namgoneka pa kama
wodzala ndi zonunkhira za mitundu mitundu, monga mwa
makonzedwe a osanganiza; ndipo anampserezera zopsereza
zambiri.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Ukoma ndi ukulu wa Yehosafati

1Ndipo Yehosafati mwana wace anakhala mfumu m'malo mwace,
nadzilimbitsa kuyambana ndi Israyeli. 2Naika ankhondo m'midzi
yonse yamalinga ya Yuda, naika aboma m'dziko la Yuda, ndi
m'midzi ya Efraimu, imene adailanda Asa atate wace. 3Ndipo
Yehova anali ndi Yehosafati, popeza anayenda m'njira zace
zoyamba za kholo lace Davide, osafuna Abaala; 4koma anafuna
Mulungu wa kholo lace nayenda m'malamulo ace, osatsata
macitidwe a Israyeli. 5Cifukwa cace Yehova anakhazikitsa ufumuwo
m'dzanja lace, ndi onse Ayuda anabwera nayo mitulo kwa
Yehosafati; ndipo zidamcurukira cuma ndi ulemu. 6Ndi mtima wace
unakwezeka m'njira za Yehova; anacotsanso misanje ndi zifanizo
m'Yuda. 7Caka cacitatu ca ufumu wace anatuma akalonga ace,
ndiwo Benihayili, ndi Obadiya, ndi Zekariya, ndi Netaneli, ndi
Mikaya, aphunzitse m'midzi ya Yuda; 8ndi pamodzi nao Alevi,
ndiwo Semaya, ndi Netaniya, ndi Zebadiya, ndi Asaheli, ndi
Semiramoti, ndi Yonatani, ndi Adoniya, ndi Tobiya, ndi Tobadoniya,
Alevi; ndi pamodzi nao Elisama ndi Yoramu, ansembe. 9Ndipo
anaphunzitsa m'Yuda ali nalo buku la cilamulo la Yehova,
nayendayenda m'midzi yonse ya Yuda, naphunzitsa mwa
anthu. 10Ndipo kuopsa kwa Yehova kunagwera maufumu a maiko
ozungulira Yuda; momwemo sanayambana ndi Yehosafati. 11Ndipo
Afilisti ena anabweca nazo kwa Yehosafati mitulo, ndi ndalama za
msonkho; Aarabu omwe anabwera nazo kwa iye zoweta, nkhosa
zamphongo zikwi zisanu ndi ziwiri mphambu mazana asanu ndi
awiri ndi atonde zikwi zisanu ndi ziwiri mphambu mazana asanu
ndi awiri. 12Ndipo Yehosafati anakula cikulire, namanga m'Yuda
nyumba zansanja, ndi midzi ya cuma. 13Nakhala nazo nchito
zambiri m'midzi ya Yuda, ndi anthu a nkhondo, ngwazi zamphamvu
m'Yerusalemu. 14Kuwerenga kwao monga mwa nyumba za atate
ao ndiko: a Yuda, akuru a zikwi; Adina wamkuru, ndi pamodzi ndi
iye ngwazi zamphamvu zikwi mazana atatu; 15ndi wotsatana naye
mkuru Yohanani, ndi pamodzi ndi iye zikwi mazana awiri mphambu
makumi asanu ndi atatu; 16ndi wotsatana naye Amasiya mwana
wa Zikri, wodzipereka kwa Yehova mwaufulu, ndi pamodzi ndi iye
ngwazi zamphamvu zikwi mazana awiri; 17ndi a Benjamini: Eliyada
ngwazi yamphamvu, ndi pamodzi ndi iye zikwi mazana awiri
ogwira mauta ndi zikopa; 18wotsatana naye Yozabadi, ndi pamodzi
ndi iye okonzekeratu ku nkhondo zikwi zana limodzi mphambu
makumi asanu ndi atatu. 19Ndiwo amene analindirira mfumu,
osawerenga iwo aja mfumu adawaika m'midzi yamalinga m'Yuda
monse.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Pangano pakati pa Yehosafati ndi Ahabu; afunsira kwa aneneri

1Yehosafati tsono anali nacocuma ndi ulemu zomcurukira, nacita
cibale ndi Ahabu. 2Ndipo zitatha zaka zina, anatsikira kwa Ahabu
ku Samariya. Ndi Ahabu anamphera iye ndi anthu anali naye
nkhosa, ndi ng'ombe zocuruka; namnyenga akwere naye pamodzi
ku Ramoti Gileadi. 3Nati Ahabu mfumu ya Israyeli kwa Yehosafati
mfumu ya Yuda, Mupita nane kodi ku Ramoti Gileadi? Nayankha,
nati, Monga inu momwemo ine; monga anthu anu momwemo
anthu anga; tidzakhala nanu ku nkhondoyi. 4Ndipo Yehosafati anati
kwa mfumu ya Israyeli, Funsiranitu mau a Yehova lero
lino. 5Pamenepo mfumu ya Israyeli anamemeza aneneri amuna
mazana anai, nanena nao, Kodi timuke kunkhondo ku Ramoti
Gileadi kapena ndileke? Ndipo anati, Kweraniko, pakuti Mulungu
adzaupereka m'dzanja la mfumu. 6Koma Yehosafati anati,
Kulibenso kuno mneneri wa Yehova, kuti tifunsire kwa iye? 7Ndipo
mfumu ya Israyeli inati kwa Yehosafati, Atsalanso munthu mmodzi,
tifunsire Yehova kwa iye; koma ndimuda, pakuti sandinenera ine
kanthu kokoma, koma zoipa nthawi zonse, ndiye Mikaya mwana
wa Yimla. Nati Yehosafati, Isatero mfumu. 8Pamenepo mfumu ya
Israyeli inaitana mdindo, niti, Katenge msanga Mikaya mwana wa
Yimla. 9Mfumu ya Israyeli tsono ndi Yehosafati mfumu ya Yuda
anakhala yense pa mpando wacifumu wace, obvala zobvala
zacifumu zao, nakhala pamalo poyera polowera pa cipata ca
Samariya; ndi aneneri onse ananenera pamaso pao. 10Ndipo
Zedekiya mwana wa Kenana anadzisulira nyanga zacitsulo, nati,
Atero Yehova, Ndi izi udzagunda Aaramu mpaka adatha psiti. 11Ndi
aneneri onse ananenera momwemo, ndi kuti, Kwerani ku Ramoti
Gileadi, mudzapindulako; pakuti Yehova adzaupereka m'dzanja la
mfumu.

Mikaya anenera motsutsana nao

12Ndipo mthenga wakukaitana Mikaya ananena naye, ndi kuti,
Taonani, mau a aneneri anenera mfumu cokoma ngati m'kamwa
m'modzi; mau anu tsono akhaletu ngati amodzi a iwowa,
nimunene cokoma. 13Nati Mikaya, Pali Yehova, conena Mulungu
wanga ndidzanena comweci. 14Pamene anafika kwa mfumu,
mfumu inanena naye, Mikaya timuke ku Ramoti Gileadi kunkhondo
kodi, kapena ndileke? Nati iye, Kwerani, mudzacita mwai; ndipo
adzaperekedwa m'dzanja lanu. 15Ndipo mfumu inati naye,
Ndikulumbiritse kangati kuti unene nane coonadi cokha cokha
m'dzina la Yehova? 16Nati iye, Ndinaona Aisrayeli onse obalalika
pamapiri ngati nkhosa zopanda mbusa; nati Yehova, Awa alibe
mbuye wao, abwerere yense ku nyumba yace

mumtendere. 17Ndipo mfumu ya Israyeli inati kwa Yehosafati,
Sindinakuuzani kuti sadzandinenera zabwino koma zoipa? 18Nati
iye, Cifukwa cace tamvani mau a Yehova, Ndinaona Yehova
alikukhala pa mpando wace wacifumu, ndi khamu lonse
lakumwamba lirikuima pa dzanja lace lamanja, ndi pa dzanja lace
lamanzere. 19Nati Yehova, Adzamnyenga Ahabu mfumu ya Israyeli
ndani, kuti akwereko, nagwe ku Ramoti Gileadi? Nati wina
mwakuti, wina mwakuti. 20Ndipo unaturuka mzimu, nuima pamaso
pa Yehova, nuti, Ndidzamnyenga ndine. Ndipo Yehova, ananena
nao, Ndi ciani? 21Nuti uwu, Ndidzaturuka ndi kukhala mzimu
wonama m'kamwa mwa aneneri ace onse. Nati Iye,
Udzamnyengadi, nudzakhoza; turuka, ukatero kumene. 22Ndipo
tsono taonani, Yehova analonga mzimu wabodza m'kamwa mwa
aneneri anu awa, nakunenetserani coipa Yehova. 23Pamenepo
Zedekiya mwana wa Kenana anayandikira, nampanda Mikaya
patsaya, nati, Mzimu wa Yehova wandicokera bwanji kulankhula
ndi iwe? 24Nati Mikaya, Tapenya, udzaona tsiku lolowa iwe
m'cipinda cam'kati kubisala. 25Ndipo mfumu ya Israyeli inati,
Mumtenge Mikaya, mukambweze kwa Amoni kazembe wa mudzi,
ndi kwa Yoasi mwana wa mfumu; 26nimuziti, Itero mfumu,
Mumuike uyu m'kaidi, ndi kumdyetsa cakudya comsautsa, ndi
kummwetsa madzi omsautsa, mpaka ndikabwera
mumtendere. 27Nati Mikaya, Mukakabwera ndi mtendere konse,
Yehova sananena mwa ine. Natiiye, Tamverani, anthu inu nonsenu.

Nkhondo iwalaka naphedwa Ahabu

28Momwemo mfumu ya Israyeli ndi Yehosafati mfumu ya Yuda
anakwera kumka ku Ramoti Gileadi. 29Ndi mfumu ya Israyeli inati
kwa Yehosafati, Ndidzadzizimbaitsa ndi kulowa kunkhondo, koma
inu bvalani zobvala zanu. Nidzizimbaitsa mfumu ya Israyeli,
namuka iwo kunkhondo. 30Mfumu ya Aramu tsono idauza akapitao
a magareta ace, ndi kuti, Musayambana ndi ang'ono kapena akuru,
koma ndi mfumu ya Israyeli yekha. 31Ndipo kunali, pamene
akapitao a magareta anaona Yehosafati, anati, Ndiye mfumu ya
Israyeli. Potero anamtembenukira kuyambana naye; koma
Yehosafati anapfuula, namthandiza Yehova; ndipo Mulungu
anawapambukitsa amleke. 32Ndipo kunali, pamene akapitao a
magareta anaona kuti sanali mfumu ya Israyeli anabwerera
osamtsatanso. 33Ndipo munthu anaponya mubvi wace
ciponyeponye, namlasa pakati pa maluma a maraya ace acitsulo.
Potero anati kwa woyendetsa garetayo, Tembenuza dzanja lako,
nundicotse ku khamu la nkhondo kuno, pakuti ndalasidwa. 34Ndipo
nkhondo inakula tsiku lija; koma mfumu ya Israyeli inagwirizizil ka
m'gareta wace popenyana ndi Aaramu mpaka madzulo, namwalira
nthawi yakulowa dzuwa.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Mneneri Yehu adzudzula Yehosafati

1Ndipo Yehosafati mfumu ya Yuda anabwerera ku nyumba yace ku
Yerusalemu mumtendere. 2Naturuka Yehu mwana wa Hanani
mlauli kukomana naye, nati kwa mfumu Yehosafati, Muyenera kodi
kuthandiza oipa, ndi kukonda amene adana ndi Yehova? Cifukwa
ca ici ukugwerani mkwiyo wocokera kwa Yehova. 3Koma zapezeka
zokoma mwa inu, popeza mwazicotsa zifanizo m'dzikomo,
mwaluniikitsanso mtima wanu kufuna Mulungu.
4Ndipo Yehosafati anakhala ku Yerusalemu, naturukiranso mwa
anthu kuyambira ku Beereseba kufikira ku mapiri a Efraimu;
nawabweza atsatenso Yehova Mulungu wa makolo ao. 5Naika
oweruza m'dziko, m'midzi yonse yamalinga ya m'Yuda, m'mudzi
m'mudzi; 6nati kwa oweruza, Khalani maso umo mucitira; pakuti
simuweruzira anthu koma Yehova; ndipo ali nanu Iyeyu
pakuweruza mlandu. 7Ndipo tsono, kuopa Yehova kukhale pa inu,
musamalire ndi kucita; pakuti palibe cosalungama kwa Yehova
Mulungu wathu, kapena kusamalira monga mwa nkhope ya
munthu, kapena kulandira mphatso. 8Yehosafati anaikanso
m'Yerusalemu Alevi, ndi ansembe ena, ndi akuru a nyumba za
makolo m'Israyeli, aweruzire Yehova, nanene mirandu. Ndipo
anabwerera kudza ku Yerusalemu. 9Ndipo anawalangiza, ndi kuti,
Muzitero ndi kuopa Yehova mokhulupirika ndi mtima
wangwiro. 10Ndipo ukakudzerani mlandu uli wonse wocokera kwa
abale anu okhala m'midzi mwao, kusiyanitsa pakati pa mwazi ndi
mwazi, pakati pa cilamulo ndi ciuzo, malemba ndi maweruzo,
muwacenjeze kuti asaparamule kwa Yehova, angafikitsire inu
nokha ndi abale anu mkwiyo; muzitero, ndipo
simudzaparamula. 11Ndipo taonani, Amariya wansembe wamkuru,
ndiye mkuru wanu m'mirandu yonse ya Yehova; ndi Zebadiya
mwana wa Ismayeli, wolamulira nyumba ya Yuda, m'mirandu
yonse ya mfumu; ndi Alevi akhale akapitao pamaso panu. Citani
molimbika mtima, ndipo Yehova akhale ndi abwino.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Yehosafati apempha Yehova pa Amoabu ndi Aamoni

1Ndipo zitatha izi, kunacitika kuti ana a Moabu, ndi ana a Amoni,
ndi ena pamodzi ndi Aamoni, anadza kuyambana nkhondo ndi
Yehosafati. 2Pamenepo anadza anthu akuuza Yehosafati, kuti,
Ukudzerani unyinji waukuru wa anthu ocokera tsidya la nyanja ku
Aramu; ndipo taonani, ali ku Hazazoni Tamara, ndiwo
Engedi. 3Ndipo Yehosafati anacita mantha, nalunjikitsa nkhope
yace kufuna Yehova, nalalikira kusala mwa Ayuda
onse. 4Namemezedwa Yuda afunsire kwa Yehova, inde anacokera
ku midzi yonse ya Yuda kufuna Yehova. 5Ndipo Yehosafati anaima
mu msonkhano wa Ayuda, ndi a ku Yerusalemu, ku nyumba ya
Yehova, pakati pa bwalo latsopano; 6nati, Yehova Mulungu wa
makolo athu, Inu sindinu Mulungu wa m'Mwamba kodi? sindinu
woweruza maufumu onse a amitundu kodi? ndi m'dzanja mwanu
muli mphamvu yolimba; palibe wina wakulaka Inu. 7Sindinu
Mulungu wathu, amene munainga nzika za m'dziko muno pa maso
pa ana anu Israyeli, ndi kulininkha kwa mbeu ya Abrahamu bwenzi
lanu kosatha? 8nakhala m'mwemo iwowa, nakumangirani
m'mwemo malo opatulika a dzina lanu, ndi kuti, 9Cikatigwera
coipa, lupanga, ciweruzo, kapena mliri, kapena njala, tidzakhala
ciriri pakhomo pa nyumba iyi, ndi pamaso panu, (pakuti m'nyumba
muno muli dzina lanu), ndi kupfuulira kwa Inu m'kusauka kwathu;
ndipo mudzamvera ndi kulanditsa. 10Ndipo tsopano, taonani ana a
Amoni, ndi Moabu, ndi a ku phiri la Seiri, amene simunalola Israyeli
awalowere, pakuturuka iwo m'dziko la Aigupto, koma
anawapambukira osawaononga; 11tapenyani, m'mene atibwezera;
kudzatiinga m'colowa canu, cimene munatipatsa cikhale colowa
cathu. 12Mulungu wathu, simudzawaweruza? pakuti mwa ife
mulibe mphamvu yakulimbana nao aunyinji ambiri awa akutidzera;
ndipo sitidziwa ngati tidzatani, koma maso athu ali kwa
Inu. 13Ndipo Ayuda onse anakhala ciriri pamaso pa Yehova,
pamodzi ndi makanda ao, akazi ao, ndi ana ao. 14Pamenepo mzimu
wa Yehova unagwera Yahazieli mwana wa Zekriya, mwana wa
Benaya, mwana wa Yetieli, mwana wa Mataniya, Mlevi, wa ana a
Asafu, pakati pa msonkhano; 15nati iye, Tamverani Ayuda inu
nonse, ndi inu okhala m'Yerusalemu, ndi inu mfumu Yehosafati,
atero nanu Yehova, Musaope musatenge nkhawa cifukwa ca
aunyinji ambiri awa; pakuti nkhondoyi si yanu, koma ya
Mulungu. 16Mawa muwatsikire; taonani, akwera pokwerera pa Zizi,
mudzakomana nao polekezera cigwa cakuno ca cipululu ca
Yerueli. 17Si kwanu kucita nkhondo kuno ai; cirimikani, imani,
nimupenye cipulumutso ca Yehova pa inu Yuda ndi Yerusalemu;
musaope, kapena kutenga nkhawa; mawa muwaturukire, popeza

Yehova ali ndi inu. 18Ndipo Yehosafati anawerama mutu wace,
nkhope yace pansi; ndi Ayuda onse, ndi okhala m'Yerusalemu
anagwa pansi pamaso pa Yehova, nalambira Yehova. 19Ndipo Alevi,
a ana a Akohati, ndi a ana a Kora, anauka kulemekeza Yehova
Mulungu wa Israyeli ndi mau omveketsa.

Amoahu ndi Aamoni akanthidwa

20Nalawira mamawa, naturuka kumka ku cipululu ca Tekoa; ndipo
poturuka iwo, Yehosafati anakhala ciriri, nati, Mundimvere ine,
Ayuda inu, ndi inu okhala m'Yerusalemu, Hmbikani mwa Yehova
Mulungu wanu, ndipo mudzakhazikika; khulupirirani aneneri ace,
ndipo mudzalemerera. 21Ndipo atafunsana ndi anthu, anaika
oyimbira Yehova, ndi kulemekeza ciyero cokometsetsa, pakuturuka
iwo kutsogolera khamu la nkhondo, ndi kuti, Yamikani Yehova,
pakuti cifundo cace cikhala cosatha. 22Ndipo poyamba iwo
kuyimba, ndi kulemekeza Yehova, anaika olalira alalire Aamoni,
Amoabu, ndi a m'phiri la Seiri, akudzera Ayuda; ndipo
anawakantha. 23Pakuti ana a Amoni, ndi a Moabu, anaukira okhala
m'phiri la Seiri, kuwapha ndi kuwaononga psiti; ndipo atatha
okhala m'Seiri, anasandulikirana kuonongana. 24Ndipo pofika
Ayuda ku dindiro la kucipululu, anapenyera aunyinjiwo; taonani,
mitembo iri ngundangunda, wosapulumuka ndi mmodzi
yense. 25Ndipo pofika Yehosafati ndi anthu ace kutenga zofunkha
zao, anapezako cuma cambiri, ndi mitembo yambiri, ndi zipangizo
zofunika, nadzifunkhira, osakhoza kuzisenza zonse; nalimkutenga
zofunkhazo masiku atatu, popeza zinacuruka. 26Ndi tsiku lacinai
anasonkhana m'cigwa ca Beraka; pakuti pamenepo analemekeza
Yehova; cifukwa cace anacha dzina lace la malowo, Cigwa ca
Beraka, mpaka lero lino. 27Pamenepo anabwerera amuna onse a
Yuda, ndi a ku Yerusalemu, nawatsogolera ndi Yehosafati,
kubwerera kumka ku Yerusalemu ndi cimwemwe; pakuti Yehova
anawakondweretsa pa adani ao. 28Ndipo anafika ku Yerusalemu ndi
zisakasa, ndi azeze, ndi malipenga, ku nyumba ya Yehova. 29Ndipo
kuopsa kwa Mulungu kunagwera maufumu onse a m'maiko,
pamene anamva kuti Yehova adayambana ndi adani a
Israyeli. 30Nucita bata ufumu wa Yehosafati; pakuti Mulungu wace
anampumulitsira pozungulirapo.

31Momwemo Yehosafati anakhala mfumu ya Yuda; anali wa zaka
makumi atatu mphambu zisanu polowa ufumu wace, nakhala
mfumu m'Yerusalemu zaka makumi awiri; ndi dzina la mace ndiye
Azuba mwana wa Sili. 32Ndipo anayenda m'njira ya Asa atate wace
osapambukamo, nacita zoongoka pamaso pa Yehova. 33Komatu
misanje siinacotsedwa; popeza pamenepo anthu sadakonzere
mitima yao kwa Mulungu wa makolo ao. 34Macitidwe ena tsono
adazicita Yehosafati, zoyamba ndi zotsiriza, taonani, zilembedwa

m'buku la mau a Yehu mwana wa Hanani, wochulidwa m'buku la mafumu a Israyeli.
35Zitathaizi, Yehosafati mfumu ya Yuda anaphatikana ndi Ahaziya mfumu ya Israyeli, yemweyo anacita moipitsitsa; 36naphatikana naye kupanga zombo zomuka ku Tarisi, nazipanga zombozo m'Ezioni Gebere. 37Pamenepo Eliezeri mwana wa Dodavahu wa Maresa ananenera kumtsutsa Yehosafati, ndi kuti, Popeza waphatikana ndi Ahaziya Yehova wapasula nchito zako. Ndipo zombo zinasweka zosakhoza kumuka ku Tarisi.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Yoramu mfumu yoipitsitsa ya Yuda

1Ndipo Yehosafati anagona pamodzi ndi makolo ace, naikidwa
pamodzi ndi makolo ace m'mudzi wa Davide; ndi Yehoramu mwana
wace anakhala mfumu m'malo mwace. 2Ndipo anali nao abale ace,
ana a Yehosafati, Azariya, ndi Yehieli, ndi Zekariya, ndi Azariya, ndi
Mikaeli, ndi Sefatiya, onsewa ndiwe ana a Yehosafati mfumu ya
Israyeli. 3Ndipo atate wao anawapatsa mphatso zazikuru, za siliva,
ndi za golidi, ndi za mtengo wace, pamodzi ndi midzi yamalinga
m'Yuda; koma ufumu anauninkha kwa Yehoramu; pakuti ndiye
mwana wace woyamba. 4Atauka tsono Yehoramu m'ufumu wa
atate wace, nadzilimbitsa, anapha ndi lupanga abale ace onse, ndi
akalonga ena omwe a Israyeli, 5Yehoramu anali wa zaka makumi
atatu mphambu ziwiri polowa ufumu wace, nacita ufumu
m'Yerusalemu zaka zisanu ndi zitatu. 6Nayenda m'njira ya mafumu
a Israyeli, umo anacitira nyumba ya Ahabu; pakuti mwana
wamkazi wa Ahabu anali mkazi wace; ndipo anacita coipa pamaso
pa Yehova. 7Koma Yehova sanafuna kuononga nyumba ya Davide
cifukwa ca pangano adalicita ndi Davide, ndi monga adalonjeza
kumpatsa iye ndi ana ace nyali nthawi zonse. 8Masiku ace Aedomu
anapanduka kucoka m'dzanja la Yuda, nadziponyera okha
mfumu. 9Ndipo Yehoramu anaoloka, ndi akazembe ace, ndi
magareta ace onse pamodzi naye, nauka usiku, nakantha Aedomu
omzinga ndi akapitao a magareta, 10Cinkana anatero, Aedomu
anapanduka kupulumuka m'dzanja la Yuda mpaka lero lino; nthawi
yomweyo anapanduka Alibina kupulumuka m'dzanja lace; cifukwa
adasiya Yehova Mulungu wa makolo ace. 11Anamanganso misanje
m'mapiri a Yuda, nacititsa okhala m'Yerusalemu cigololo,
nakankhirako Ayuda. 12Ndipo anamdzera kalata wofuma kwa Eliya
mneneri, ndi kuti, Atero Yehova Mulungu wa Davide atate wanu,
Popeza simunayenda m'njira za Yehosafati atate wanu, kapena
m'njira za Asa mfumu ya Yuda, 13koma mwayenda m'njira ya
mafumu a Israyeli, ndi kucititsa Yuda ndi okhala m'Yerusalemu
cigololo, monga umo anacitira cigololo a nyumba ya Ahabu,
mwaphanso abale anu a nyumba ya atate wanu, ndiwo abwino
akuposa inu; 14taonani, Yehova adzakantha anthu anu, ndi ana
anu, ndi akazi anu, ndi cuma canu conse, makanthidwe
akuru; 15ndipo mudzadwala kwakukuru nthenda yamatumbo,
mpaka matumbo anu adzaturuka cifukwa ca nthendayi tsiku ndi
tsiku. 16Ndipo Yehova anautsira Yehoramu mzimu wa Afilisti, ndi wa
Aarabu okhala pambali pa Akusi; 17ndiwo anakwerera Yuda,
nathyolamo, nalanda cuma conse cinapezeka m'nyumba ya
mfumu, ndi ana ace omwe, ndi akazi ace, osamsiyira mwana,
koma Yehoahazi yekha mwana wace wamng'ono. 18Ndi pambuyo

pace pa izi zonse Yehova anamdwalitsa m'matumbo ace ndi nthenda yosacira nayo. 19Ndipo kunali, itapita nthawi, pakutha pace pa zaka ziwiri, anaturuka matumbo ace mwa nthenda yace namwalira nazo nthenda zoipa, Ndipo anthu ace sanampserezera zonunkhira, monga umo anapserezera makolo ace. 20Anali wa zaka makumi atatu mphambu ziwiri polowa ufumu wace, nakhala mfumu m'Yerusalemu zaka zisanu ndi zitatu, namuka wopanda wina womlakalaka; ndipo anamuika m'mudzi wa Davide, koma si m'manda a mafumu ai.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Ahaziya mfumu ya Yuda aphedwa ndi Yehu

1Ndipo okhala m'Yerusalemu anamlonga Ahaziya mwana wace
wamng'ono akhale mfumu m'malo mwace; pakuti gulu la anthu,
adadzawo pamodzi ndi Aarabu kucigono, adapha ana oyamba
onse. Momwemo Ahaziya mwana wa Yehosafati anakhala mfumu
ya Yuda. 2Ahaziya anali wa zaka makumi anai mphambu ziwiri
polowa ufumu wace, nakhala mfumu m'Yerusalemu caka cimodzi;
ndi dzina la mace ndiye Ataliya mwana wa Omri. 3Iyenso anayenda
m'njira za nyumba ya Ahabu; pakuti wompangira ndi mace acite
coipa, 4Ndipo anacita coipa pamaso pa Yehova, monga umo
anacitira a nyumba ya Ahabu; pakuti ompangira ndi iwowa,
atamwalira atate wace; ndi kuonongeka kwace
nkumeneko. 5Anayendanso m'kupangira kwao, namuka pamodzi
ndi Yehoramu mwana wa Ahabu mfumu ya Israyeli, kukayambana
nkhondo ndi Hazaeli mfumu ya Aramu ku Ramoti Gileadi; ndipo
Aaramu anamlasa Yehoramu. 6Nabwerera iye kuti amcize ku
Yezreeli, apole mabala amene adamkantha ku Rama, pamene
anayambana ndi Hazaeli mfumu ya Aramu, Ndipo Azariya mwana
wa Yehoramu mfumu yaYuda anatsikira kukaona Yehoramu mwana
wa Ahabu m'Yezreeli, popeza anadwala. 7Kuonongeka kwa Ahaziya
tsono nkwa Mulungu, kuti amuke kwa Yehocamu; pakuti atafika
anaturukira pamodzi ndi Yehoramu kukayambana ndi Yehu mwana
wa Nimsi, amene Yehova anamdzoza alikhe nyumba ya
Ahabu. 8Ndipo kunali, pakulanga Yehu nyumba ya Ahabu, anapeza
akalonga a Israyeli, ndi ana a abale a Ahaziya, akutumikira
Ahaziya, nawapha. 9Atatero, anafunafuna Ahaziya, namgwira
alikubisala m'Samariya, nabwera naye kwa Yehu, namupha; ndipo
anamuika; pakuti anati, Ndiye mwana wa Yehosafati, wofuna
Yehova ndi mtima wace wonse. Ndipo panalibe wina wa nyumba ya
Ahaziya wa mphamvu yakusunga ufumuwo.

Ataliya apha acifuma onse, Yoasi apulumuka

10Pamene Ataliya anaona kuti mwana wace adafa, anauka,
naononga mbeu yonse yacifumu ya nyumba ya Yuda. 11Koma
Yehosafati mwana wamkazi wa mfumu anatenga Yoasi mwana wa
Ahaziya, namuba pakati pa ana a mfumu ophedwa, namlonga iye
ndi mlezi wace m'cipinda cogonamo. Momwemo Yehosafati mwana
wamkazi wa mfumu Yehoramu, mkazi wa Yehoyada wansembe
(popeza ndiye mlongo wace wa Ahaziya), anambisira Ataliya,
angamuphe. 12Ndipo iye anali nao wobisika m'nyumba ya Mulungu
zaka zisanu ndi cimodzi; nakhala Ataliya mfumu yaikazi ya dziko.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Yehoyada adzoza Yoasi akhale mfumu

1Koma caka cacisanu ndi ciwiri Yehoyada anadzilimbitsa natenga
atsogoleri a mazana, Azariya mwana wa Yeroamu, ndi Ismayeli
mwana wa Yohanana, ndi Azariya mwana wa Obedi, ndi Maaseya
mwana wa Adaya, ndi Elisafati mwana wa Zikiri, apangane naye
pamodzi. 2Ndipo iwo anayendayenda mwa Yuda, nasonkhanitsa
Alevi m'midzi yonse ya Yuda, ndi akuru a nyumba za makolo
m'Israyeli; nadza iwo ku Yerusalemu. 3Ndipo msonkhano wonse
unapangana pangano ndi mfumu m'nyumba ya Mulungu. Ndipo
ananena nao, Taonani, mwana wa mfumu adzakhala mfumu
monga Yehova ananena za ana a Davide. 4Cimene muzicita ndi ici:
limodzi la magawo atatu mwa inu olowera dzuwa la Sabata, la
ansembe ndi Alevi, akhale olindirira pakhomo; 5ndi limodzi la
magawo atatu likhale ku nyumba ya mfumu; ndi limodzi la
magawo atatu ku cipata ca maziko; ndi anthu onse akhale
m'mabwalo a nyumba ya Yehova. 6Koma asalowe mmodzi
m'nyumba ya Yehova, ansembe okha, ndi Alevi otumikira, alowe
iwowa; pakuti ndiwo opatulika; koma anthu onse asunge udikiro wa
Yehova. 7Ndipo Alevi amzinge mfumu pozungulirapo, yense ndi
zida zace m'dzanja mwace; ndipo ali yense wolowa m'nyumba
aphedwe; nimukhale inu pamodzi ndi mfumu pakulowa ndi
pakuturuka iye. 8Momwemo Alevi ndi Ayuda onse anacita monga
mwa zonse anawauza Yehoyada wansembe; natenga yense amuna
ace alowe dzuwa la Sabata pamodzi ndi oturuka dzuwa la Sabata;
pakuti Yehoyada wansembe sanamasula zigawo. 9Ndi Yehoyada
wansembe anapereka kwa akazembe a mazana mikondo, ndi
zikopa, ndi maraya acitsulo, zinali za mfumu Davide, zokhala
m'nyumba, ya Mulungu. 10Ndipo anaika anthu onse, yense ndi cida
cace m'dzanja lace, amzinge mfumu, kuyambira mbali ya ku
dzanja lamanja la nyumba kufikira mbali ya ku dzanja lamanzere la
nyumba, kuloza ku guwa la nsembe ndi kunyumba. 11Pamenepo
anaturutsa mwana wa mfumu, nambveka korona, nampatsa
mboni, namlonga ufumu; ndi Yehoyada ndi ana ace anamdzoza,
nati, Ikhale ndi moyo mfumu.

Aphedwa Ataliya

12Ndipo pamene Ataliya anamva phokoso la anthu alikuthamanga
ndi kulemekeza mfumu, anadza kwa anthu m'nyumba ya
Yehova; 13napenya, ndi kuona mfumu inaima pa nsanamira yace
polowera; ndi atsogoleri, ndi malipenga, anali kwa mfumu; ndi
anthu onse a m'dziko anakondwera, naomba amalipenga; oyimbira
omwe analiko ndi zoyimbirazo, nalangiza poyimbira colemekeza.
Pamenepo Ataliya anang'amba zobvala zace, nati, Ciwembu,
ciwembu. 14Koma Yehoyada wansembe anaturuka nao atsogoleri a

mazana akuyang'anira khamu la nkhondo, nanena nao, Mturutseni mkaziyo pakati pa mipambo; ndipo ali yense womtsata aphedwe ndi lupanga; pakuti wansembe adati, Msamphere m'nyumba ya Yehova. 15Ndipo anampisa malo; namuka iye kolowera ku cipata ca akavalo kunyumba ya mfumu; ndi pomwepo anamupha.

Pangano la Yehoyadawansembe

16Ndipo Yehoyada anacita pangano pakati pa iye, ndi anthu onse, ndi mfumu, kuti adzakhala anthu a Yehova. 17Ndi anthu onse anamuka ku nyumba ya Baala, naipasula, naphwanya maguwa ace a nsembe, ndi mafano ace; namupha Matana wansembe wa Baala ku maguwa a nsembe. 18Ndipo Yehoyada anaika mayang'aniro a nyumba ya Yehova m'dzanja la ansembe Aleviwo, amene Davide anawagawa, ayang'anire nyumba ya Yehova; napereka nsembe zopsereza za Yehova monga mulembedwa m'cilamulo ca Mose, ndi kukondwera ndi kuyimbira, monga mwa cilangizo ca Davide. 19Ndipo anaika odikira ku makomo a nyumba ya Yehova, kuti wodetsedwa nako kanthu kali konse asalowemo. 20Natenga atsogoleri a mazana, ndi omveka, ndi akazembe a anthu, ndi anthu onse a m'dziko, natsika ndi mfumu ku nyumba ya Yehova; nalowera pa cipata ca kumtunda m'nyumba ya mfumu, namkhalitsa mfumu pa mpando wa ufumu. 21Ndipo anthu onse a m'dziko anakondwera; ndi m'mudzi munali cete, atamupha Ataliya ndi lupanga.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Yoasi akonzanso Kacisi

1Yoasi anali wa zaka zisanu ndi ziwiri polowa ufumu wace, nakhala
mfumu m'Yerusalemu zaka makumi anai; ndi dzina la mace ndiye
Zibiya wa ku Beereseba. 2Ndipo Yoasi anacita zoongoka pamaso pa
Yehova masiku onse a Yehoyada wansembe. 3Ndipo Yehoyada
anamtengera akazi awiri, nabala ana amuna ndi akazi. 4Ndipo
pambuyo pace mumtima mwa Yoasi munali cofuna kukonzanso
nyumba ya Yehova. 5Nasonkhanitsa ansembe ndi Alevi, nanena
nao, Muturuke kumka ku midzi ya Yuda, ndi kusonkhanitsa kwa
Aisrayeli onse ndarama zakukonzetsa nyumba ya Mulungu wanu
caka ndi caka; ndipo inu fulumirani nayo nchitoyi. Koma Alevi
sanafulumira nayo. 6Ndipo mfumu inaitana Yehoyada mkuru wao,
niti naye, Unalekeranji kuuza Alevi abwere nao kucokera m'Yuda
ndi Yerusalemu msonkho wa Mose mtumiki wa Yehova, ndi wa
msonkhano wa Israyeli, ukhale wa cihema ca umboni? 7Pakuti ana
a Ataliya mkazi woipa uja anathyola citseko ca nyumba ya
Mulungu, natenga zopatulidwa zonse za nyumba ya Yehova
kuzipereka kwa Baala. 8Nilamulira mfumu, ndipo anapanga bokosi,
naliika kunja ku cipata ca nyumba ya Yehova. 9Nalalikira mwa Yuda
ndi Yerusalemu, abwere nao kwa Yehova msonkho umene Mose
mtumiki wa Mulungu anauikira Aisrayeli m'cipululu. 10Ndipo
akalonga onse ndi anthu onse anakondwera, nabwera nazo,
naponya m'bokosi mpaka atatha. 11Ndipo kunali, pamene
amabwera nalo bokosi alipenye mfumu, mwa manja a Alevi,
nakapenya kuti ndalama zinacurukamo, amadza mlembi wa
mfumu, ndi kapitao wa wansembe wamkulu, nakhutula za
m'bokosi, nalisenza ndi kubwera nalo kumalo kwace. Anatero tsiku
ndi tsiku, nasonkhanitsa ndalama zocuruka. 12Ndipo mfumu ndi
Yehoyada anazipereka kwa iwo akugwira nchito ya utumiki ya
nyumba ya Yehova, nalembera amisiri omanga ndi miyala, ndi
osema mitengo, akonzenso nyumba ya Yehova; ndiponso akucita
ndi citsulo ndi mkuwa alimbitse nyumba ya Yehova. 13Momwemo
anacita ogwira nchito, nikula nchito mwa dzanja lao, nakhazikitsa
iwo nyumba ya Mulungu monga mwa maonekedwe ace,
nailimbitsa. 14Ndipo ataitsiriza, anabwera nazo ndalama zotsala
kwa mfumu ndi Yehoyada, napanga nazo zipangizo za nyumba ya
Yehova, zipangizo za kutumikira nazo, ndi kupereka nsembe nazo,
ndi zipande, ndi zipangizo za golidi ndi siliva. Ndipo anapereka
kosalekeza nsembe zopsereza m'nyumba ya Yehova masiku onse a
Yehoyada.

Anthu apatukira mafano

15Koma Yehoyada anakalamba, nacuruka masiku, namwalira iye;
ndiye wa zaka zana limodzi mphambu makumi atatu pamene

anamwalira. 16Ndipo anamuika m'mudzi wa Davide, pakati pa
mafumu; pakuti anacita zabwino m'Israyeli, ndi kwa Mulungu, ndi
ku nyumba yace. 17Atamwalira Yehoyada tsono, akalonga a Yuda
anadza, nalambira mfumu. Ndipo mfumu inawamvera. 18Ndipo
anasiya nyumba ya Yehova Mulungu wa makolo ao, natumikira
zifanizo, ndi mafano; ndipo mkwiyo unawagwera Yuda ndi
Yerusalemu, cifukwa ca kuparamula kwao kumene. 19Koma Iye
anawatumira aneneri kuwabwezeranso kwa Yehova, ndiwo
anawacitira umboni; koma sanawamvera.

Zekariya adzudzula anthu naphedwa

20Ndipo mzimu wa Mulungu unabvala Zekariya mwana wa
Yehoyada wansembe, naima iye kumtunda kwa anthu, nanena
nao, Atero Mulungu, Mulakwiranji malamulo a Yehova kuli
kosalemerera nako? Popeza mwasiya Yehova, Iye wasiyanso
inu. 21Koma anampangira ciwembu, namponya miyala, mwa
lamulo la mfumu m'bwalo la nyumba ya Yehova. 22Motero mfumu
Yoasi sanakumbukila zokoma anamcitirazi Yehoyada atate wace,
koma anapha mwana wace; ndiye pomwalira anati, Yehova
acipenye, nacifunse. 23Ndipo kunacitika, podzanso nyengoyi
khamu la nkhondo la Aaramu linamkwerera, nafika iwo ku Yuda ndi
Yerusalemu, naononga mwa anthu akalonga onse a anthu,
natumiza zofunkha zao zonse kwa mfumu ya ku
Damasiko. 24Pakuti khamu la nkhondo la Aaramu linadza la anthu
owerengeka; ndipo Yehova anapereka khamu lalikuru m'dzanja lao;
popeza adasiya Yehova Mulungu wa makolo ao. Motero anacitira
Yoasi zomlanga. 25Ndipo atamcokera (popeza anamsiya wodwala
nthenda zazikuru), anyamata ace anamcitira ciwembu, cifukwa ca
mwazi wa ana a Yehoyada wansembe, namupha pakama pace,
namwalira iye; ndipo anamuika m'mudzi wa Davide, koma
osamuika m'manda a mafumu. 26Omcitira ciwembu ndi awa:
Zabadi, mwana wa Simeati wamkazi M-amoni; ndi Yozabadi,
mwana wa Simiriti wamkazi Mmoabu. 27Za ana ace tsono, ndi
katundu wamkuru anamsenza, ndi kumanganso kwa nyumba ya
Mulungu, taonani, zilembedwa m'buku lomasulira la mafumu.
Ndipo Amaziya mwana wace anakhala mfumu m'malo mwace.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Amaziya agonjetsa Aedomu

1Amaziya anali wa zaka makumi awiri mphambu zisanu polowa
ufumu wace, nakhala mfumu m'Yerusalemu zaka makumi awiri
mphambu zisanu ndi zinai; ndi dzina la mace ndiye Yehoadana wa
ku Yerusalemu. 2Ndipo anacita zoongoka pamaso pa Yehova, koma
wosacita ndi mtima wangwiro. 3Kunacitika tsono, utamkhazikikira
ufumu, anapha anyamata ace amene adapha mfumu atate
wace. 4Koma sanapha ana ao, koma anacita monga umo
mulembedwa m'cilamulo, m'buku la Mose, monga Yehova
analamulira, ndi kuti, Atate asafere ana, ndi ana asafere atate;
koma yense afere chimo lace lace. 5Ndipo Amaziya anamemeza
Ayuda, nawaika monga mwa nyumba za atate ao, atsogoleri a
zikwi, ndi atsogoleri a mazana, ndiwo onse a Yuda ndi Benjamini;
nawawerenga a zaka makumi awiri ndi mphambu, nawapeza
amuna osankhika zikwi mazana atatu akuturukira kunkhondo,
ogwira mkondo ndi cikopa. 6Analemberanso ngwazi zamphamvu za
m'Israyeli zikwi zana limodzi, kuwalipira matalente a siliva zana
limodzi. 7Koma anamdzera munthu wa Mulungu, kuti, Mfumu,
khamu la nkhondo la Israyeli lisapite nanu; pakuti Yehova sakhala
ndi Israyeli, sakhala ndi ana onse a Efraimu. 8Koma ngati mumuka,
citani, limbikani kunkhondo, Mulungu adzakugwetsani pamaso pa
adani; pakuti Mulungu ali nayo mphamvu yakuthandiza ndi
yakugwetsa. 9Ndipo Amaziya anati kwa munthu wa Mulungu, Koma
nanga titani nao matalente zana limodzi ndinapatsa ankhondo a
Israyeli? Nati munthu wa Mulungu, Yehova ali nazo zoposa izi
kukupatsani. 10Pamenepo Amaziya anawapambutsa, ndiwo
ankhondo anamdzera kucokera ku Efraimu, amuke kwao; potero
adapsa mtima kwambiri pa Yuda, nabwera kwao ndi kutentha
mtima. 11Nalimbika mtima Amaziya, natsogolera anthu ace,
namuka ku Cigwa ca Mcere, nakantha ana a Seiri zikwi
khumi. 12Ndi ana a Yuda anagwira zikwi khumi ena amoyo,
nabwera nao pamwamba pa thanthwe, nawakankha pamwamba
pa thanthwe, naphwanyika onsewo. 13Koma amuna a nkhondo
amene Amaziya anawabwereretsa, kuti asamuke naye kunkhondo,
anagwera midzi ya Yuda kuyambira Samariya kufikira Betihoroni,
nakantha a iwowa zikwi zitatu, nalanda zofunkha zambiri.

Amaziya alangidwa popembedza mafano

14Ndipo kunali, atafika Amaziya atatha kuwapha Aedomu, ndi
kubwera nayo milungu ya ana a Seiri, anaiika ikhale milungu yace,
naigwadira, naifukizira, 15Pamenepo mkwiyo wa Mulungu
unayakira Amaziya, ndipo anamtumira mneneri amene anati,
Mwafuniranji milungu ya anthu imene siinalanditsa anthu ao
m'dzanja lanu? 16Ndipo kunali, pakulankhula naye mfumu, inanena

naye, Takuika kodi ukhale wopangira mfumu? leka, angakukanthe. Pamenepo mneneriyo analeka, nati, Ndidziwa kuti Mulungu watsimikiza mtima kukuononga ni, popeza mwacita ici ndi kusamvera kupangira kwanga.
17Pamenepo Amaziya mfumu ya Yuda anafunsana ndi ompangira, natumiza kwa Yoasi mwana wa Yehoahazi mwana wa Yehu mfumu ya Israyeli, ndi kuti, Idzani, tionane maso. 18Ndi Yoasi mfumu ya Israyeli anatumiza kwa Amaziya mfumu ya Yuda ndi kuti, Mtungwi wa ku Lebano unatumiza kwa mkungudza wa ku Lebano, ndi kuti, Mpatse mwana wanga wamwamuna mwana wako wamkazi akhale mkazi wace; koma nyama ya kuthengo ya ku Lebano inapitapo, nipondereza mtungwi. 19Mukuti, Taonani, ndakantha Aedomu, nukwezeka mtima wanu kudzikuza; khalani kwanu tsopano, mungadziutsire tsoka, mungagwe, inu, ndi Yuda pamodzi ndi inu. 20Koma wosamvera Amaziya, pakuti nca Mulungu ici kuti awapereke m'dzanja la adani ao; popeza anafuna milungu ya Edomu. 21Motero anakwera Yoasi mfumu ya Israyeli, ndipo iye ndi Amaziya mfumu ya Yuda anapenyana maso ku Betisemesi, ndiwo wa Yuda. 22Nakanthidwa Yuda pamaso pa Israyeli, nathawa yense kuhema kwace. 23Ndipo Yoasi mfumu ya Israyeli anagwira Amaziya mfumu ya Yuda, mwana wa Yoasi mwana wa Yehoahazi, ku Betisemesi, nabwera naye ku Yerusalemu, nagamula linga la Yerusalemu kuyambira cipata ca Efraimu kufikira cipata ca kungondya, mikono mazana anai. 24Natenga golidi ndi siliva zonse, ndi zipangizo zonse zopezeka m'nyumba ya Mulungu kwa Obedi Edomu, ndi cuma ca nyumba ya mfumu, acikole omwe; nabwerera kumka ku Samariya.
25Ndipo Amaziya mwana wa Yoasi mfumu ya Yuda anakhala ndi moyo, atamwalira Yoasi mwana wa Yehoahazi mfumu ya Israyeli, zaka khumi ndi zisanu. 26Macitidwe ena tsono a Amaziya, oyamba ndi otsiriza, taonani, salembedwa kodi m'buku la mafumu a Yuda ndi Israyeli? 27Ndipo cipambukire Amaziya kusatsata Yehova, anamcitira ciwembu m'Yerusalemu, nathawira ku Lakisi iyeyu; koma anatuma omtsatira ku Lakisi, namupha komweko. 28Namnyamula pa akavalo, namuika pamodzi ndi makolo ace m'mudzi wa Yuda.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Uziyaagonjetsa adani ambiri

1Ndipo anthu onse Ayuda anatenga Uziya, ndiye wa zaka khumi
mphambu zisanu ndi cimodzi, namlonga ufumu m'malo mwa atate
wace Amaziya. 2Iye anamanga Eloti, naubweza kwa Yuda, mfumu
itagona ndi makolo ace. 3Uziya anali wa zaka khumi mphambu
zisanu ndi cimodzi polowa ufumu wace, nakhala mfumu
m'Yerusalemu zaka makumi asanu mphambu ziwiri; ndi dzina la
mace ndiye Yekoliya wa ku Yerusalemu. 4Nacita iye zoongoka
pamaso pa Yehova, monga mwa zonse adazicita atate wace
Amaziya. 5Ndipo iye anali munthu wakufuna Mulungu masiku a
Zekariya, ndiye wozindikira masomphenya a Mulungu; ndipo
masiku akufunira Yehova iye, Mulungu anamlemereza; 6popeza
anaturuka, nayambana ndi Afilisti, nagamula linga la Gati, ndi linga
la Yabine, ndi linga la Asidodi; namanga midzi m'dziko la Asidodi,
ndi mwa Afilisti. 7Ndipo Mulungu anamthandiza poyambana ndi
Afilisti, ndi Aarabu okhala m'Guribaala, ndi Ameuni. 8Ndipo Aamoni
anampatsa Uziya mitulo; ndi dzina lace linabuka mpaka polowera
ku Aigupto; pakuti analil mbika cilimbikire. 9Uziya anamanganso
nsanja m'Yerusalemu pa cipata ca kungondya, ndi pa cipata ca
kucigwa, ndi popindika linga; nazilimbikitsa. 10Namanga nsanja
m'cipululu, nakumba zitsime zambiri; popeza anali nazo zoweta
zambiri; kumadambo, ndi kuzidikha; nakhala nao olima minda, ndi
osunga mpesa kumapiri ndi ku nthaka yopatsa bwino; pakuti ndiye
mlimi. 11Uziya anali nalonso khamu la anthu a nkhondo, oturuka
kunkhondo magulu; nawawerenga monga mwa mawerengedwe ao
ndi dzanja la mlembi Yeyeli, ndi kapitao Maseya, monga anawauza
Hananiya kazembe wina wa mfumu. 12Ciwerengo conse ca akuru a
nyumba za makolo, ndiwo ngwazi zamphamvu, ndico zikwi ziwiri
mphambu mazana asanu ndi limodzi. 13Ndipo m'dzanja mwao
munali khamu la nkhondo zikwi mazana atatu mphambu zikwi
zisanu ndi ziwiri kudza mazana asanu ocita nkhondo ndi mphamvu
yaikuru, kuthandiza mfumu alimbane ndi adani. 14Ndipo Uziya
anawakonzeratu ankhondo onse zikopa, ndi mikondo, ndi zisoti
zacitsulo, ndi maraya acitsulo, ndi mauta, ndi miyala
yoponyera. 15Napanga m'Yerusalemu makina, opangidwa ndi eni
luso, akhale pansanja ndi kungondya, aponye nao mibvi ndi miyala
yaikuru. Ndi dzina lace linamveka kutali; pakuti anathandizidwa
modabwiza, mpaka analimbikatu.

Uziva alakwa ku Kacisi nasanduka wakhate

16Koma atakhala wamphamvu, mtima wace unakwezeka
momuononga, nalakwira Yehova Mulungu wace; popeza analowa
m'Kacisi wa Yehova kufukiza pa guwa la nsembe la
cofukiza. 17Ndipo Azariya wansembe analowa pambuyo pace, ndi

pamodzi naye ansembe a Yehova makumi asanu ndi atatu, ndiwo olimba mtima; 18natsutsana ndi mfumu Uziya, nati kwa iye, Sikuyenera inu, Uziya, kufukizira Yehova, koma ansembe, ana a Aroni opatulidwira kufukiza; turukani m'malo opatulika; pakuti mwalakwa; Yehova Mulungu sakulemekezanipo. 19Koma Uziya anapsa mtima, mbale ya zofukiza iri m'dzanja lace kufukiza nayo; ndipo pakupsa mtima nao ansembe, khate linabuka pamphumi pace, pamaso pa ansembe m'nyumba ya Yehova, pambali pa guwa lofukizapo. 20Ndipo Azariya wansembe wamkulu, ndi ansembe onse, anampenya, ndi kuona kuti anali wakhate pamphumi pace namkankhiza msanga kubwalo; nafulumiranso yekha kuturukako, pakuti Yehova adamkantha. 21Ndipo mfumu Uziya anali wakhate mpaka tsiku la imfa yace, nakhala m'nyumba ya padera, popeza ndiye wakhate; pakuti anadulidwa ku nyumba ya Yehova; ndi Yotamu mwana wace anayang'anira nyumba ya mfumu naweruza anthu a m'dziko. 22Macitidwe ena tsono a Uziya, oyamba ndi otsiriza, anawalemba Yesaya mneneri mwana wa Amosi. Ndipo Uziya anagona ndi makolo ace, namuika ndi makolo ace kumanda kwa mafumu; pakuti anati, Ndiye wakhate; ndi Yotamu mwana wace anakhala mfumu m'malo mwace.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Yotamu mfumu ya Yuda

1Yotamu anali wa zaka makumi awiri, mphambu zisanu polowa
ufumu wace, nakhala mfumu m'Yerusalemu zaka khumi ndi zisanu
ndi cimodzi; ndi dzina la mace ndiye Yerusa mwana wa
Zadoki. 2Ndipo anacita zoongoka pamaso pa Yehova, monga umo
adacitira atate wace Uziya; pokhapo sanalowa m'Kacisi wa Yehova.
Koma anthu anacitabe zobvunda. 3Anamanga cipata ca kumtunda
ca nyumba ya Yehova, ndi pa linga la Ofeli anamanga
kwakukuru. 4Namanga midzi m'mapiri a Yuda, ndi m'nkhalango
anamanga nyumba zansanja, ndi nsanja zomwe. 5Anayambananso
ndi mfumu ya ana a Amoni, namgonjetsa, Ndi ana a Amoni
anamninkha caka comweci matalente a siliva zana limodzi, ndi
miyeso ya tirigu zikwi khumi, ndi ya barele zikwi khumi. Ana a
Amoni anabwera nazo zomwezo kwa iye caka caciwiri ndi cacitatu
comwe. 6Momwemo Yotamu anakula mphamvu, popeza anakonza
njira zace pamaso pa Yehova Mulungu wace. 7Macitidwe ena tsono
a Yotamu, ndi nkhondo zace zonse, ndi njira zace, taonani,
zalembedwa m'buku la mafumu a Israyeli ndi Yuda. 8Anali wa zaka
makumi awiri mphambu zisanu polowa ufumu wace, nakhala
mfumu m'Yerusalemu zaka khumi mphambu zisanu ndi
cimodzi. 9Ndipo Yotamu anagona ndi makolo ace, namuika
m'mudzi wa Davide; ndi Ahazi mwana wace anakhala mfumu
m'malo mwace.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Ahazi mfumu yoipitsitsa ya Yuda

1Ahazi anali wa zaka makumi awiri polowa ufumu wace, nakhala
mfumu m'Yerusalemu zaka khumi mphambu zisanu ndi cimodzi;
koma sanacita zoongoka pamaso pa Yehova ngati Davide kholo
lace, 2koma anayenda m'njira za mafumu a Israyeli, napangiranso
Abaala mafano oyenga, 3Nafukizanso yekha m'cigwa ca mwana wa
Hinomu, napsereza ana ace m'moto, monga mwa zonyansa za
amitundu, amene Yehova anawainga pamaso pa ana a
Israyeli. 4Naphera nsembe, nafukiza kumisanje, ndi kuzitunda, ndi
patsinde pa mtengo uli wonse wogudira. 5Cifukwa cace Yehova
Mulungu wace anampereka m'dzanja la mfumu ya Aramu; ndipo
anamkantha, natenga ndende unyinji waukuru wa anthu ace,
nafika nao ku Damasiko. Anaperekedwanso iye m'dzanja la mfumu
ya Israyeli, amene anamkantha makanthidwe akuru. 6Pakuti Peka
mwana wa Remaliya anapha ku Yuda tsiku limodzi zikwi zana
limodzi ndi makumi awiri, ngwazi zonsezo; popeza adasiya Yehova
Mulungu wa makolo ao. 7Ndipo Zikiri munthu wamphamvu wa
Efraimu anapha Maseya mwana wa mfumu, ndi Azrikamu
woyang'anira nyumba, ndi Elikana wotsatana ndi mfumu. 8Ndipo
ana a Israyeli anatenga ndende ena a abale ao zikwi mazana awiri,
akazi, ana amuna ndi akazi, nalandanso kwa iwo zofunkha zambiri,
nabwera nazo zofunkhazo ku Samariya, 9Koma panali mneneri wa
Yehova pomwepo, dzina lace Odedi; naturuka iye kukomana nayo
nkhondo ikudzayo ku Samariya, nanena nao, Taonani, popeza
Yehova Mulungu wa makolo anu anakwiya ndi Yuda, anawapereka
m'dzanja lanu, nimunawapha ndi kupsa mtima kofikira
kumwamba. 10Ndipo tsopano mukuti mugonjetse ana a Yuda ndi
Yerusalemu akhale akapolo ndi adzakazi anu; palibe nanunso kodi
mirandu yoparamula kwa Yehova Mulungu wanu? 11Mundimvere
tsono, bwezani andende amene munawatenga ndende a abale
anu; pakuti mkwiyo waukali wa Yehova uli pa inu. 12Pamenepo
akuru ena a ana a Efraimu, Azariya mwana wa Yohanana, Berekiya
mwana wa Mesilemoti, ndi Yehizikiya mwana wa Salumu, ndi
Amasa mwana wa Hadilai, anaukira aja ofuma
kunkhondo, 13nanena nao, Musalowa nao andende kuno; pakuti inu
mukuti mutiparamulitse kwa Yehova, kuonjezera pa macimo athu
ndi zoparamula zathu; pakuti taparamula kwakukuru, ndipo pali
mkwiyo waukali pa Israyeli. 14Pamenepo eni zida anasiya andende
ndi zofunkha pamaso pa akalonga ndi msonkhano
wonse. 15Nanyamuka amuna ochulidwa maina, natenga andende,
nabveka ausiwa onse mwa iwo ndi zofunkhazo, nawapatsa
zobvala, ndi nsapato, nawadyetsa ndi kuwamwetsa, nawadzoza,

nasenza ofoka ao onse pa aburu, nafika nao ku Yeriko, mudzi wa migwalangwa, kwa abale ao; nabwerera iwo kunka ku Samariya.
16Nthawi yomweyi mfumu Ahazi anatumiza kwa mafumu a Asuri amthandize. 17Pakuti Aedomu anadzanso, nakantha Yuda, natenga andende. 18Afilisti omwe adagwa m'midzi ya kucidikha, ndi ya kumwela kwa Yuda, nalanda Betisemesi, ndi Azaloni, ndi Gederoti, ndi Soko ndi miraga yace, ndi Timna ndi miraga yace; nakhala iwo komweko. 19Pakuti Yehova anacepetsa Yuda cifukwa ca Ahazi mfumu ya Israyeli; popeza iye anacita comasuka pakati pa Yuda, nalakwira Yehova kwambiri. 20Ndipo Tigilati Pilesere mfumu ya Asuri anadza kwa iye, namsautsa osamlimbikitsa. 21Pakuti Ahazi analandako za m'nyumba ya Yehova ndi za m'nyumba ya mfumu, ndi ya akalonga, nazipereka kwa mfumu ya Asuri, osathandizidwa nazo. 22Ndipo nthawi ya nsautso yace anaonjeza kulakwira Yehova, mfumu Ahazi yemweyo. 23Popeza anaphera nsembe milungu ya Damasiko yomkantha, nati, Popeza milungu ya mafumu a Aramu iwathandiza, ndiiphere nsembe, indithandize inenso. Koma inamkhumudwitsa iye, ndi Aisrayeli onse. 24Ndipo Ahazi anasonkhanitsa zipangizo za m'nyumba ya Mulungu, naduladula zipangizo za m'nyumba ya Mulungu, natseka pa makomo a nyumba ya Yehova, nadzimangira maguwa a nsembe m'ngondya ziri zonse za Yerusalemu. 25Ndi m'midzi iri yonse ya Yuda anamanga misanje ya kufukizira milungu yina, nautsa mkwiyo wa Yehova Mulungu wa makolo ace. 26Macitidwe ena tsono, ndi njira zace zonse, zoyamba ndi zotsiriza, taonanani, zilembedwa m'buku la mafumu a Yuda ndi Israyeli. 27Ndi Ahazi anagona ndi makolo ace, namuika m'mudzi wa Yerusalemu; pakuti sanadza naye ku manda a mafumu a Israyeli; ndipo Hezekiya mwana wace anakhala mfumu m'malo mwace.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Hezekiya mfumu ya Yuda

1Hezekiya analowa ufumu wace ali wa zaka makumi awiri mphambu zisanu,
nakhala mfumu m'Yerusalemu zaka makumi awiri mphambu zisanu ndi zinai;
ndi dzina la mace ndiye Abiya mwana wa Zekariya. 2Nacita iye zoongoka
pamaso pa Yehova, monga umo monse adacitira Davide kholo lace. 3Caka
coyamba ca ufumu wace, mwezi woyamba, anatsegula pa makomo a nyumba
ya Yehova, napakonzanso. 4Nalowetsa ansembe ndi Alevi, nawasonkhanitsa
pamalo poyera kum'mawa, 5nanena nao, Ndimvereni, Alevi inu, dzipatuleni,
nimupatule nyumba ya Yehova Mulungu wa makolo anu, ndi kucotsa zoipsa
m'malo opatulika. 6Pakuti analakwa makolo athu, nacita coipa pamaso pa
Yehova Mulungu wathu, namsiya, natembenuza nkhope zao osapenya
cokhalamo Yehova, namfulatira. 7Anatsekanso pa khomo la likole, nazima
nyalizo, osafukizanso zonunkhira kapena kupereka nsembe zopsereza m'malo
opatulika kwa Mulungu wa Israyeli. 8Motero mkwiyo wa Yehova unali pa Yuda
ndi Yerusalemu, nawapereka anjenjemere, nakhale codabwiza ndi
cotsonyetsa, monga umo muonera m'maso mwanu. 9Pakuti taonani, makolo
athu adagwa ndi lupanga, ndi ana athu amuna ndi akazi ndi akazi athu ali
andende cifukwa ca ici. 10Tsono mumtima mwanga nditi ndicite cipangano ndi
Yehova Mulungu wa Israyeli, kuti mkwiyo wace waukali utembenuke
kuticokera. 11Ana anga, musazengereza tsopano; popeza Yehova
anakusankhani inu muime pamaso pace, kumtumikira Iye, ndi kuti mukhale
atumiki ace ndi kufukiza zonunkhira.

Alevi ayeretsa Kacisi

12Pamenepo ananyamuka Alevi, Mahati mwana wa Amasai ndi Yoeli mwana
wa Azariya, a ana a Akohati; ndi a ana a Merari, Kisi mwana wa Abidi, ndi
Azariya mwana wa Yehaleleli; ndi a Agerisoni, Yowa mwana wa Zima, ndi
Edeni mwana wa Yowa; 13ndi a ana a Elizafana, Simri ndi Yeueli; ndi a ana a
Asafu, Zekariya ndi Mataniya; 14ndi a ana a Hemani, Yehudi ndi Simei ndi a
ana a Yedutuni, Semaya ndi Uziyeli, 15Ndipo anamemeza abale ao,
nadzipatula, nalowa monga adawauza mfumu mwa mau a Yehova, kuyeretsa
nyumba ya Yehova. 16Ndipo ansembe analowa m'kati mwace mwa nyumba ya
Yehova kuiyeretsa, naturutsira ku bwalo la nyumba ya Yehova zoipsa zonse
anazipeza m'Kacisi wa Yehova. Nazilandira Alevi, kuziturutsira kunja ku
mtsinje wa Kedroni. 17Anayamba tsono kuipatula tsiku loyamba la mwezi
woyamba, nafikira ku likole la Yehova tsiku lacisanu ndi citatu la mwezi,
naipatula nyumba ya Yehova m'masiku asanu ndi atatu; natsiriza tsiku
lakhumi ndi cisanu ndi cimodzi. 18Pamenepo analowa m'katimo kwa mfumu
Hezekiya, nati, Tayeretsa nyumba yonse ya Yehova, ndi guwa la nsembe
yopsereza, ndi zipangizo zace zonse, ndi gome la mkate woonekera, ndi
zipangizo zace zonse. 19Zipangizo zonse zomwe adazitaya mfumu Ahazi
m'ufumu wace m'kulakwa kwace kuja, tazikonza, ndi kuzipatula; ndipo
taonani, ziri ku guwa la nsembe la Yehova.

Hezekiya aikanso cipembedzo ca Yehova

20Pamenepo mfumu Hezekiya analawira mamawa, nasonkhanitsa akalonga a
m'mudzi, nakwera kumka ku nyumba ya
Yehova. 21Ndipoanabweranazong'ombe zisanundi ziwiri, ndi nkhosa
zamphongo zisanu ndi ziwiri ndi ana a nkhosa asanu ndi awiri, ndi atonde
asanu ndi awiri, zikhale nsembe yaucimo ya ufumu, ndi ya malo opatulika, ndi
ya Yuda. Ndipo anawauza ansembe ana a Aroni azipereke pa guwa la nsembe
la Yehova. 22Momwemo anapha ng'ombezo, ndi ansembe analandira mwazi,
nauwaza pa guwa la nsembe, napha nkhosa zamphongozo, nawaza mwazi pa

guwa la nsembe; anaphanso ana a nkhosawo, nawaza mwazi pa guwa la nsembe. 23Pamenepo anayandikiza nao atonde a nsembe yaucimo pamaso pa mfumu ndi msonkhano; ndipo iwo anawasanjika manja ao, 24ndi ansembewo anawapha, nacita nsembe yaucimo ndi mwazi wao pa guwa la nsembe, kucita cotetezera Aisrayeli onse; pakuti mfumu idauza kuti nsembe yopsereza ndi nsembe yaucimo zikhale za Aisrayeli onse. 25Ndipo anaika Alevi m'nyumba ya Yehova ndi nsanje, ndi zisakasa, ndi azeze, monga umo adauzira Davide, ndi Gadi mlauli wa mfumu, ndi Natani mneneriyo; pakuti lamulo ili lidafuma kwa Yehova mwa aneneri ace. 26Alevi tsono anaimirira ndi zoyimbira za Davide, ndi ansembe anakhala ndi malipenga. 27Nanena Hezekiya kuti apereke nsembe yopsereza pa guwa la nsembe. Ndipo pakuyamba nsembe yopsereza, inayambanso nyimbo ya Yehova ndi malipenga, pamodzi ndi zoyimbira za Davideyo mfumu ya Israyeli. 28Ndi msonkhano wonse unalambira, ndi oyimbira anayimba, ndi amalipenga anaomba; zonsezi mpaka adatsiriza nsembe yopsereza. 29Ndipo atatsiriza kuperekaku, mfumu ndi onse opezeka pamodzi naye anawerama, nalambira. 30Hezekiya mfumu ndi akalonga anauzanso Alevi ayimbire Yehova zomlemekeza ndi mau a Davide ndi a Asafu mlauli. Ndipo anayimbira zomlemekeza mokondwera, nawerama mitu yao, nalambira. 31Pamenepo Hezekiya anayankha, nati, Tsopano mwadzipatulira kwa Yehova, senderani, bwerani nazo nsembe zophera ndi nsembe zoyamika ku nyumba ya Yehova. Ndi msonkhano unabwera nazo nsembe zophera ndi nsembe zoyamika, ndi onse a mtima wofuna mwini anabwera nazo nsembe zopsereza. 32Ndi kuwerenga kwace kwa nsembe zopsereza unabwera nazo msonkhanowo ndiko ng'ombe makumi asanu ndi awiri, nkhosa zamphongo zana limodzi, ndi ana a nkhosa mazana awiri; zonsezi nza nsembe yopsereza ya Yehova. 33Ndi zinthu, zopatulika zinafikira ng'ombe mazana asanu ndi limodzi, ndi nkhosa zikwi zitatu. 34Koma ansembe anaperewera, osakhoza kusenda nsembe zonse zopsereza; m'mwemo abale ao Alevi anawathandiza, mpaka idatha nchitoyi, mpaka ansembe adadzipatula; pakuti Alevi anaposa ansembe m'kuongoka mtima kwao kudzipatula. 35Ndiponso zidacuruka nsembe zopsereza, pamodzi ndi mafuta a nsembe zamtendere, ndi nsembe zothira za nsembe yopsereza iri yonse. Momwemo utumiki wa nyumba ya Yehova unalongosoka. 36Nakondwera Hezekiya ndi anthu onse pa ici Mulungu adakonzeratu; pakuti cinthuci cidacitika modzidzimutsa.

Hezekiya acita Paskha ku Yerusalemu

1Ndipo Hezekiya anatumiza kwa Israyeli ndi Yuda onse,
nalembanso akalata kwa Efraimu ndi Manase, kuti abwere ku
nyumba ya Yehova ku Yerusalemu, kucitira Yehova Mulungu wa
Israyeli Paskha. 2Pakuti mfumu idapangana ndi akuru ace, ndi
msonkhano wonse wa m'Yerusalemu, kuti acite Paskha mwezi
waciwiri. 3Pakuti sanakhoza kumcita nthawi ija, popeza ansembe
odzipatulira sanafikira, ndi anthu sadasonkhana ku
Yerusalemu. 4Ndipo cinthuci cinayenera m'maso mwa mfumu ndi
msonkhano wonse. 5Motero anakhazikitsa mau kulalikira mwa
Israyeli lonse, kuyambira Beereseba kufikira ku Dani, kuti abwere
kucitira Yehova Mulungu wa Israyeli Paskha ku Yerusalemu; pakuti
nthawi yaikuru sanacita monga mudalembedwa. 6Tsono amtokoma
anamuka ndi akalata ofuma kwa mfumu ndi akuru ace mwa
Israyeli ndi Yuda lonse, monga inauza mfumu ndi kuti, Inu ana a
Israyeli, bwerani kwa Yehova Mulungu wa Abrahamu, Isake, ndi
Israyeli, kuti Iye abwere kwa otsala anu opulumuka m'dzanja la
mafumu a Asuri. 7Ndipo musamakhala ngati makolo anu ndi abale
anu, amene anai akwira Yehova Mulungu wa makolo ao, motero
kuti anawapereka apasuke, monga mupenya, 8Musamakhala ouma
khosi monga makolo anu; koma gwiranani dzanja ndi Yehova,
nimulowe m'malo ace opatulika, amene anapatula kosatha, ndi
kutumikira Yehova Mulungu wanu; kuti mkwiyo wace waukali
utembenuke kwa inu. 9Pakuti mukabwera kwa Yehova, abale anu
ndi ana anu adzapeza cifundo pamaso pa iwo anawatenga ndende,
nadzalowanso m'dziko muno; pakuti Yehova Mulungu wanu ngwa
cisomo ndi cifundo; sadzakuyang'anirani kumbali ngati mubwera
kwa Iye, 10Ndipo amtokoma anapitira m'midzi m'midzi mwa dziko
la Efraimu ndi Manase, mpaka Zebuloni; koma anawaseka
pwepwete nawanyodola. 11Komatu ena a Aseri ndi Manase ndi a
Zebuloni anadzicepetsa, nadza ku Yerusalemu. 12Ku Yuda komwe
kunali dzanja la Mulungu lakuwapatsa mtima umodzi, kucita
cowauza mfumu ndi akuru mwa mau a Yehova. 13Nasonkhana ku
Yerusalemu anthu ambiri kucita madyerero a mkate wopanda
cotupitsa mwezi waciwiri, msonkhano waukuru ndithu. 14Ndipo
anauka nacotsa maguwa a nsembe okhala m'Yerusalemu, nacotsa
pofukizira zonunkhira, naziponya m'mtsinje wa
Kedroni. 15Pamenepo anaphera Paskha tsiku lakhumi ndi cinai la
mwezi waciwiri, ndipo ansembe ndi Alevi anacita manyazi,
nadzipatula, nabwera nazo nsembe zopsereza ku nyumba ya
Yehova. 16Naima m'malo mwao mwa kulongosoka kwao, monga
mwa cilamulo ca Mose munthu wa Mulunguyo; ansembe anawaza
mwazi, ataulandira ku dzanja la Alevi. 17Pakuti munali ambiri

mumsonkhano sanadzipatula; potero Alevi anayang'anira kupha za Paskha kwa ali yense wosakhala woyera, kuwapatulira Yehova. 18Pakuti, anthu aunyinji, ndiwo ambiri a Efraimu, ndi Manase, Isakara, ndi Zebuloni, sanadziyeretsa, koma anadya Paskha mosati monga munalembedwa. 19Koma Hezekiya anawapempherera, ndi kuti, Yehova wabwino akhululukire yense wakuika mtima wace kufuna Mulungu Yehova, Mulungu wa makolo ace, cinkana sanayeretsedwa monga mwa mayeretsedwe a malo opatulika. 20Ndipo Yehova anamvera Hezekiya, nawaciritsa anthu. 21Ndipo ana a Israyeli opezeka m'Yerusalemu anacita madyerero a mkate wopanda cotupitsa masiku asanu ndi awiri ndi cimwemwe cacikuru; ndi Alevi ndi ansembe analemekeza Yehova tsiku ndi tsiku ndi zoyimbira zakuliritsa kwa Yehova. 22Ndipo Hezekiya ananena motonthoza mtima kwa Alevi onse akuzindikira bwino za utumiki wa Yehova. Ndipo anadya pamkomano masiku asanu ndi awiri, naphera nsembe zoyamika, ndi kulemekeza Yehova Mulungu wa makolo ao. 23Ndipo msonkhano wonse unapangana kucita masiku asanu ndi awiri ena, nacita masiku asanu ndi awiri ena ndi cimwemwe. 24Pakuti Hezekiya mfumu ya Yuda anapatsa msonkhano ng'ombe cikwi cimodzi, ndi nkhosa zikwi zisanu ndi ziwiri; ndi akuru anapatsa msonkhano ng'ombe cikwi cimodzi, ndi nkhosa zikwi khumi; ndipo ansembeambiri adadzipatula, 25Ndi msonkhano wonse wa Yuda, pamodzi ndi ansembe ndi Alevi, ndi msonkhano wonse wocokera kwa Israyeli, ndi alendo ocokera ku dziko la Israyeli, ndi okhala m'Yuda, anakondwera. 26Momwemo munali cimwemwe cacikuru m'Yerusalemu; pakuti kuyambira masiku a Solomo mwana wa Davide mfumu ya Israyeli simunacitika cotero m'Yerusalemu. 27Pamenepo ansembe Alevi anauka, nadalitsa anthu; ndi mau ao anamveka, ndi pemphero lao lidakwera pokhala pace popatulika Kumwamba.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Afafaniza cipembedzo conse ca mafano

1Citatha ici conse tsono, Aisrayeli onse opezekako anaturuka
kumka ku midzi ya Yuda, naphwanya zoimiritsa, nalikha zifanizo,
nagamula misanje ndi maguwa a nsembe m'Yuda monse, ndi
m'Benjamini, m'Efraimunso, ndi m'Manase, mpaka adaziononga
zonse. Pamenepo ana onse a Israyeli anabwerera, yense ku dziko
lace ndi ku midzi yao.
2Ndipo Hezekiya anaika zigawo za ansembe ndi Alevi, monga mwa
magawidwe ao, yense monga mwa utumiki wace, ndi ansembe ndi
Alevi, acite nsembe zopsereza ndi nsembe zoyamika kutumikira,
ndi kuyamika, ndi kulemekeza, ku zipata za cigono ca
Ambuye. 3Naikanso gawo la mfumu lotapa pa cuma cace la
nsembe zopsereza, ndilo la nsembe zopsereza za m'mawa ndi
madzulo, ndi la nsembe zopsereza za masabata, ndi za pokhala
mwezi, ndi za nyengo zoikika, monga mulembedwa m'cilamulo ca
Yehova. 4Anauzanso anthu okhala m'Yerusalemu apereke gawo la
ansembe ndi Alevi, kuti iwowa alimbike m'cilamulo ca
Yehova. 5Ndipo pobuka mau aja, ana a Israyeli anapereka
mocuruka, zobala zoyamba za tirigu, vinyo, ndi mafuta, ndi uci, ndi
za zipatso zonse za m'minda, ndi limodzi la magawo khumi la
zonse anabwera nazo mocuruka. 6Ndi ana a Israyeli ndi Yuda
okhala m'midzi ya Yuda, iwonso anabwera nalo limodzi la magawo
khumi la ng'ombe, ndi nkhosa, ndi limodzi la magawo khumi la
zinthu zopatulika, zopatulikira Yehova Mulungu wao; naziunjika
miyuru miyuru, 7Mwezi wacitatu anayamba kuika miyalo ya
miyuruyi, naitsiriza mwezi wacisanu ndi ciwiri. 8Ndipo pamene
Hezekiya ndi akuru ace anadza, naona miyuruyi, analemekeza
Yehova, nadalitsa anthu ace Aisrayeli. 9Pamenepo Hezekiya
anafunsana ndi ansembe ndi Alevi za miyuruyi, 10Ndipo Azariya
wansembe wamkuru wa nyumba ya Zadoki anamyankha, nati,
Ciyambire anthu anabwera nazo zopereka ku nyumba ya Yehova,
tadya, takhuta, ndipo zatitsalira zambiri; pakuti Yehova anadalitsa
anthu ace; ndipo suku kucuruka kwa cotsala. 11Pamenepo
Hezekiya anawauza akonze zipinda m'nyumba ya Yehova;
nazikonza. 12Ndipo anabwera nazo nsembe zokweza, ndi amodzi a
magawo khumi, ndi zinthu zopatulika, mokhulupirika; ndi mkuru
woyang'anira izi ndiye Konaniya Mlevi, ndi Simei mng'ono wace
ndiye wotsatana naye. 13Ndi Yeiyeli, ndi Azaziya, ndi Nahati, ndi
Asaheli, ndi Yerimoti, ndi Yozabadi, ndi Eliyeli, ndi Ismakiya, ndi
Mahati, ndi Benaya, ndiwo akapitao omvera Konaniya ndi Simei
mng'ono wace, oikidwa ndi Hezekiya mfumu ndi Azariya mkuru wa
ku nyumba ya Mulungu. 14Ndipo Kore mwana wa Imna Mlevi, wa ku
cipata ca kum'mawa, anayang'anira zopereka zaufulu za Mulungu,

kugawira nsembe zokweza za Yehova, ndi zopatulikitsa. 15Ndi
omvera iye ndiwo Edeni, ndi Minyamini, ndi Yesuwa; ndi Semaya,
Amariya, ndi Sekaniya, m'midzi ya ansembe, kugawira abale ao
m'zigawo zao mokhulupirika, akuru monga ang'ono; 16pamodzi ndi
iwo oyesedwa mwa cibadwidwe ca amuna, kuyambira a zaka zitatu
ndi mphambu, kwa ali yense amene adalowa m'nyumba ya
Yehova, monga mwa nchito yace pa tsiku lace, kukacita za utumiki
wao m'udikiro wao monga mwa zigawo zao; 17ndi iwo oyesedwa
mwa cibadwidwe ca ansembe mwa nyumba za makolo ao, ndi
Alevi, kuyambira a zaka makumi awiri ndi mphambu m'udikiro
mwao, monga mwa zigawo zao; 18ndi iwo oyesedwa mwa
cibadwidwe ca ana ao ang'ono onse, akazi ao, ndi ana ao amuna
ndi akazi, mwa msonkhano wonse; pakuti m'kukhulupirika kwao
anadzipatula akhale opatulika; 19panalinso amuna mwa ana a
Aroni ansembe, okhala m'minda ya kubusa kwa midzi yao,
m'mudzi uli wonse, ochulidwa maina ao, agawire amuna onse mwa
ansembe, ndi onse mwa Alevi, oyesedwa mwa cibadwidwe
magawo ao. 20Momwemo anacita Hezekiya mwa Yuda lonse nacita
cokoma, ndi coyenera, ndi cokhulupirika, pamaso pa Yehova
Mulungu wace. 21Ndipo m'nchito iri yonse anaiyamba m'utumiki
wa nyumba ya Mulungu, ndi m'cilamulo, ndi m'mauzo, kufuna
Mulungu wace, anacita ndi mtima wace wonse, nalemerera nayo.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Sanakeribu agwera Yuda

1Zitatha zinthu izi zokhulupirika, anadza Sanakeribu mfumu ya
Asuri, nalowera Yuda, namangira midzi yamalinga misasa, nati
adzigonjetsere iyi. 2Ndipo pakuona Hezekiya kuti wadza
Sanakeribu, ndi kuti nkhope yace inalunjikitsa kuyambana nkhondo
ndi Yerusalemu, 3anapangana ndi akuru ace ndi amphamvu ace,
kutseka madzi a m'akasupe okhala kunja kwa mudzi; namthandiza
iwo. 4Nasonkhana anthu ambiri, natseka akasupe onse, ndi mtsinje
woyenda pakati pa dziko, ndi kuti, Angafike mafumu a Asuri ndi
kupeza madzi ambiri. 5Ndipo analimbika mtima, namangitsa linga
lonse mopasuka, nalikweza mpaka pansanja, ndi linga lina kunja
kwace, nalimbitsa Milo m'mudzi wa Davide, napanga zida ndi
zikopa zocuruka. 6Naika akazembe a nkhondo alamulire anthu,
nawasonkhanitsira kuli iye ku bwalo la ku cipata ca mudzi, nanena
nao motonthoza mtima wao ndi kuti, 7Limbani, mulimbike mtima,
musaopa kapena ku tenga nkhawa pankhope pa mfumu ya Asuri
ndi aunyinji okhala naye; pakuti okhala nafe acuruka koposa
okhala naye; 8pamodzi ndi iye pali dzanja la thupi lanyama; koma
pamodzi ndi ife pali Yehova Mulungu wathu, kutithandiza ndi
kutigwirira nkhondo. Ndipo anthu anacirikizika ndi mau a Hezekiya
mfumu ya Yuda.
9Pambuyo pace Sanakeribu mfumu ya Asuri, akali ku Lakisi ndi
mphamvu yace yonse pamodzi naye, anatuma anyamata kwa
Hezekiya mfumu ya Yuda, ndi kwa Ayuda onse okhala ku
Yerusalemu, ndi kuti, 10Atero Sanakeribu mfumu ya Asuri, Mutama
ciani kuti mukhala m'linga m'Yerusalemu? 11Sakukopani Hezekiya,
kuti akuperekeni mufe nayo njala ndi ludzu, ndi kuti, Yehova
Mulungu wathu adzatilanditsa m'dzanja la mfumu ya
Asuri? 12Sanaicotsa misanje yace ndi maguwa ace a nsembe
Hezekiya yemweyo, nauza Yuda ndi Yerusalemu, ndi kuti,
Mugwadire ku guwa la nsembe limodzi ndi kufukiza zonunkhira
pamenepo? 13Simudziwa kodi comwe ine ndi makolo anga tacitira
anthu onse a m'maikomo? Kodi milungu ya mitundu ya anthu
inakhoza konse kulanditsa dziko lao m'dzanja langa? 14Ndi uti mwa
milungu yonse ya mitunduyi ya anthu, amene makolo anga
anawaononga konse, unakhoza kulanditsa anthu ace m'dzanja
mwanga, kuti Mulungu wako adzakhoza kukulanditsa iwe m'dzanja
mwanga? 15Ndipo tsono, asakunyengeni Hezekiya, ndi kukukopani
motero, musamkhulupirira; pakuti palibe mulungu wa mtundu uli
wonse wa anthu, kapena ufumu uli wonse, unakhoza kulanditsa
anthu ace m'dzanja mwanga; ndipo kodi Mulungu wanu
adzakulanditsani inu m'dzanja langa? 16Ndipo anyamata ace
anaonjeza kunena motsutsana ndi Yehova Mulungu, ndi mnyamata

wace Hezekiya, 17Analemberanso akalata a kunyoza Yehova
Mulungu wa Israyeli, ndi kunena motsutsana ndi Iye, ndi kuti,
Monga milungu ya mitundu ya anthu a m'maiko, imene
siinalanditsa anthu ao m'dzanja langa, momwemo Mulungu wa
Hezekiya sadzalanditsa anthu ace m'dzanja mwanga. 18Ndipo
anapfuula ndi mau akuru m'cinenedwe ca Ayuda kwa anthu a
m'Yerusalemu okhala palinga, kuwaopsa ndi kuwabvuta, kuti
alande mudziwu. 19Nanenera Mulungu wa Yerusalemu, monga umo
amanenera milungu ya mitundu ya anthu a pa dziko lapansi, ndiyo
nchito ya manja a anthu. 20Ndipo Hezekiya mfumu, ndi Yesaya
mneneri mwana wa Amozi, anapemphera pa ici, napfuulira
Kumwamba. 21Ndipo Yehova anatuma wamthenga amene
anaononga ngwazi zamphamvu zonse, ndi atsogoleri, ndi
akazembe, ku cigono ca mfumu ya Asuri. Nabwerera iye ndi
nkhope yamanyazi ku dziko lace. Ndipo atalowa m'nyumba ya
mulungu wace, iwo oturuka m'matumbo mwace anamupha ndi
lupanga pomwepo. 22Momwemo Yehova analanditsa Hezekiya ndi
okhala m'Yerusalemu m'dzanja la Sanakeribu mfumu ya Asuri, ndi
m'dzanja la onse ena, nawatsogolera monsemo. 23Ndipo ambiri
anabwera nayo mitulo kwa Yehova ku Yerusalemu, ndi za mtengo
wace, kwa Hezekiya mfumu ya Yuda; nakwezeka iye pamaso pa
amitundu onse kuyambira pomwepo.

Nthenda ndi imfa ya Hezekiya

24Masiku omwe aja Hezekiya anadwala pafupi imfa; ndipo
anapemphera kwa Yehova; ndi Iye ananena naye, nampatsa
cizindikilo codabwiza. 25Koma Hezekiya sanabwezera monga mwa
cokoma anamcitira, pakuti mtima wace unakwezeka; cifukwa cace
unamdzera mkwiyo iye, ndi Yuda, ndi Yerusalemu. 26Koma
Hezekiya anadzicepetsa m'kudzikuza kwa mtima wace, iye ndi
okhala m'Yerusalemu, momwemo mkwiyo wa Yehova sunawadzera
masiku a Hezekiya. 27Ndipo cuma ndi ulemu zinacurukira
Hezekiya, nadzimangira iye zosungiramo siliva, ndi golidi, ndi
timiyala ta mtengo wace, ndi zonunkhira, ndi zikopa, ndi zipangizo
zokoma ziri zonse; 28ndi nyumba zosungiramo zipatso za tirigu, ndi
vinyo, ndi mafuta, ndi zipinda za nyama iri yonse, ndi makola a
zoweta. 29Nadzimangiranso midzi, nadzionera nkhosa ndi ng'ombe
zocuruka; pakuti Mulungu adampatsa cuma
cambirimbiri. 30Hezekiya yemweyo anatseka kasupe wa kumtunda
wa madzi a Gihoni, nawapambutsa atsikire ku madzulo kwa mudzi
wa Davide. Ndipo Hezekiya analemerera nazo nchito zace
zonse. 31Koma pokhala naye akazembe a akalonga a ku Babulo,
amene anatumiza kwa iye kufunsira za codabwiza cija cidacitika
m'dzikomo, Mulungu anamsiya, kumuyesa, kuti adziwe zonse za
mumtima mwace. 32Macitidwe ena tsono a Hezekiya, ndi nchito

zace zokoma, taonani, zilembedwa m'masomphenya a Yesaya mneneri mwana wa Amozi, ndi m'buku la mafumu a Yuda ndi Israyeli. 33Ndipo Hezekiya anagona ndi makolo ace, namuika polowerera ku manda a ana a Davide; ndi Ayuda onse ndi okhala m'Yerusalemu anamcitira ulemu pa imfa yace. Ndipo Manase mwana wace anakhala mfumu m'malo mwace.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Manase aikanso cipembedza ca mafano

1Manase anali wa zaka khumi ndi ziwiri polowa ufumu wace,
nakhala mfumu m'Yerusalemu zaka makumi asanu mphambu
zisanu. 2Nacita coipa pamaso pa Yehova, monga mwa zonyansa za
amitundu, amene Yehova anawacotsa m'dziko mwao pamaso pa
ana a Israyeli. 3Pakuti anamanganso misanje adaipasula Hezekiya
atate wace, nautsira Abaala maguwa a nsembe, napanga zifanizo,
nalambira khamu lonse la kuthambo, nalitumikira. 4Namanga
maguwa a nsembe m'nyumba ya Yehova, imene Yehova adati,
M'Yerusalemu mudzakhala dzina langa ku nthawi
zonse. 5Namangiranso khamu lonse la kuthambo maguwa a
nsembe m'mabwalo awiri a nyumba ya Yehoya. 6Anapititsanso ana
ace pamoto m'cigwa ca ana a Hinomu, naombeza maula,
nasamalira malodza, nacita zanyanga, naika obwebweta ndi
openduza; anacita zoipa zambiri pamaso pa Yehova kuutsa mkwiyo
wace. 7Ndipo anaika cifanizo cosema ca fanolo adacipanga
m'nyumba ya Mulungu, imene Mulungu adati kwa Davide ndi
Solomo mwana wace, M'nyumba muno ndi m'Yerusalemu umene
ndausankha m'mafuko onse a Israyeli ndidzaika dzina langa ku
nthawi zonse; 8ndipo sindidzasunthanso phazi la Israyeli ku dziko
ndaliikira makolo anu; pokhapo asamalire kucita zonse
ndawalamulira, cilamulo conse, ndi malemba, ndi maweruzo, mwa
dzanja la Mose. 9Koma Manase analakwitsa Yuda ndi okhala
m'Yerusalemu, kotero kuti anacita coipa koposa amitundu, amene
Yehova anawaononga pamaso pa ana a Israyeli.

Manase atengedwa kunka ku Babulo, alapa nabwezedwa ku Yerusalemu

10Ndipo Yehova analankhula ndi Manase ndi anthu ace, koma
sanasamalira. 11Motero Yehova anawafikitsira akazembe a khamu
la nkhondo la mfumu ya Asuri, namgwira Manase ndi zokowera,
nammanga matangadza, namuka naye ku Babulo. 12Ndipo
popsinjika iye anapembedza Yehova Mulungu wace, nadzicepetsa
kwambiri pamaso pa Mulungu wa makolo ace. 13Anampempha,
ndipo anapembedzeka, namvera kupembedza kwace, nambwezera
ku Yerusalemu m'ufumu wace. Pamenepo anadziwa Manase kuti
Yehova ndiye Mulungu.
14Citatha ici tsono iye anaumangira mudzi wa Davide linga lakunja,
kumadzulo kwa Gihoni, m'cigwa, mpaka polowera pa cipata
cansomba; nazinga Ofeli, nalikweza kwambiri; anaikanso
akazembe a nkhondo m'midzi yonse yamalinga ya m'Yuda. 15Ndipo
anacotsa milungu yacilendo, ndi fanoli m'nyumba ya Yehova, ndi
maguwa onse a nsembe anawamanga m'phiri la nyumba ya
Yehova ndi m'Yerusalemu, nawataya kunja kwa mudzi. 16Namanga

guwa la nsembe la Yehova, napherapo nsembe zamtendere ndi zoyamika, nalamulira Yuda atumikire Yehova Mulungu wa Israyeli. 17Koma anthu anapherabe nsembe pamisanje; koma anaziphera Yehova Mulungu wao. 18Macitidwe ena tsono a Manase, ndi pemphero lace kwa Mulungu wace, ndi mau a alauli akunena naye m'dzina la Yehova Mulungu wa Israyeli, taonani, zalembedwa m'niacitidwe a mafumu a Israyeli. 19Pemphero lace lomwe, ndi m'mene Mulungu anapembedzeka naye, ndi chimo lace lonse, ndi kulakwa kwace, ndi apo anamanga misanje, naimika zifanizo ndi mafano osema asanadzicepetse, taonani, zalembedwa m'buku la mau a Hozai. 20Momwemo Manase anagona ndi makolo ace, namuika m'nyumba mwace mwace; ndi Amoni mwana wace anakhala mfumu m'malo mwace.

Amoni mfumu yoipayo

21Amoni ndiye wa zaka makumi awiri mphambu ziwiri polowa ufumu wace, nakhala mfumu m'Yerusalemu zaka ziwiri. 22Ndipo anacita coipa pamaso pa Yehova, monga umo anacitira Manase atate wace; pakuti Amoni anaphera nsembe mafano osema onse amene adawapanga Manase atate wace, nawatumikira. 23Koma sanadzicepetsa pamaso pa Yehova, monga umo anadzicepetsera Manase atate wace; koma Amoni amene anacurukitsa kuparamula kwace. 24Ndipo anyamata ace anampangira ciwembu, namupha m'nyumba yace yace. 25Koma anthu a m'dziko anapha onse adampangira ciwembu mfumu Amoni; ndi anthu a m'dziko analonga Yosiya mwana wace akhale mfumu m'malo mwace.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Yosiya acotsa cipembedzo ca mafano, nakonzanso Kacisi

1Yosiya ndiye wa zaka zisanu ndi zitatu polowa ufumu wace,
nakhala mfumu m'Yerusalemu zaka makumi atatu mphambu
cimodzi. 2Nacita zoongoka pamaso pa Yehova, nayenda m'njira za
Davide kholo lace, osapambuka ku dzanja lamanja kapena
kulamanzere. 3Pakuti atakhala mfumu zaka zisanu ndi ziwiri akali
mnyamata, anayamba kufuna Mulungu wa Davide kholo lace;
ndipo atakhala zaka khumi ndi cimodzi anayamba kuyeretsa Yuda
ndi Yerusalemu, kuzicotsa misanje, ndi zifanizo, ndi mafano osema,
ndi mafano oyenga, 4Ndipo anthu anagumula maguwa a nsembe a
Abaala pamaso pace; nawalikha mafano a dzuwa anakwezeka
pamwamba pao; naphwanya zifanizo, ndi mafano osema, ndi
mafano oyenga; nazipera, naziwaza pamanda pa iwo amene
adaziphera nsembe. 5Napsereza mafupa a ansembe pa maguwa a:
nsembe ao, nayeretsa Yuda ndi Yerusalemu. 6Nateronso m'midzi ya
Manase, ndi Efraimu, ndi Simeoni, mpaka Nafitali, m'mabwinja
mwao mozungulira. 7Nagumula maguwa a nsembe, naperapera
zifanizo ndi mafano osema, nalikha mafano a dzuwa onse m'dziko
lonse la Israyeli, nabwerera kumka ku Yerusalemu.
8Atakhala mfumu tsono zaka khumi mphambu zisanu ndi ziwiri,
atayeretsa dziko ndi nyumbayi, anatuma safana mwana wa
Azaliya, ndi Maseya kazembe wa mudzi, ndi Yona mwana wa
Yoadazi wolemba mbiri, akonze nyumba ya Yehova Mulungu
wace. 9Ndipo anadza kwa Hilikiya wansembe wamkulu, napereka
ndarama adabwera nazo ku nyumba ya Mulungu, zimene Alevi
osunga pakhomo adasonkhanitsa kuzilandira ku dzanja la Manase
ndi Efraimu, ndi kwa otsala onse a Israyeli, ndi kwa Yuda yense, ndi
Benjamini, ndi kwa okhala m'Yerusalemu. 10Ndipo anazipereka
m'dzanja la anchito oikidwa ayang'anire nyumba ya Yehova; ndi
iwo anazipereka kwa anchito akucita m'nyumba ya Yehova,
kukonza ndi kulimbitsa nyumbayi; 11anazipereka kwa amisiri a
mitengo ndi omanga nyumba, agule miyala yosema, ndi mitengo
ya mitanda yam'mwamba ndi yammunsi ya nyumbazi,
adaziononga mafumu a Yuda. 12Ndipo amunawo anacita nchitoyi
mokhulupirika; ndi oikidwa awayang'anire ndiwo Yohati ndi
Obadiya, Alevi, a ana a Merari; ndi Zekariya ndi Mesulamu, a ana a
Akohati, kuifulumiza; ndi Alevi ena ali yense wa luso la
zoyimbira, 13Anayang'aniranso osenza akatundu, nafulumiza onse
akugwira nchito ya utumiki uli wonse; ndi mwa Alevi munali
alembi, ndi akapitao, ndi odikira.

Hilikiya apeza buku la cilamulo

14Ndipo pakuturutsa ndarama zimene adalowa nazo ku nyumba ya
Yehova, Hilikiya wansembe anapeza buku la cilamulo la Yehova

mwa dzanja la Mose. 15Ndipo Hilikiya anayankha nati kwa Safani
mlembi, Ndapeza buku la cilamulo m'nyumba ya Yehova. Hilikiya
napereka buku kwa Safani. 16Ndi Safani anamuka nalo buku kwa
mfumu, nabwezeranso mau kwa mfumu, ndi kuti, Zonse
mudazipereka kwa anyamata anu alikuzicita. 17Nakhuthula
ndarama zinapezeka m'nyumba ya Yehova, nazipereka m'manja a
akapitao ndi m'manja a anchito. 18Ndipo Safani mlembi anauza
mfumu, ndi kuti, Hilikiya wansembe anandipatsa buku.
Nawerengamo Safani pamaso pa mfumu. 19Ndipo kunali, atamva
mfumu mau a cilamulo, anang'amba zobvala zace. 20Mfumu niuza
Hilikiya, ndi Ahikamu mwana wa Safani, ndi Abidoni mwana wa
Mikaya, ndi Safani mlembi, ndi Asaya mnyamata wa mfumu, ndi
kuti, 21Mukani, mundifunsire kwa Yehova, ine ndi otsala m'Israyeli
ndi Yuda, za mau a m'buku lopezekalo; pakuti ukali wa Yehova
atitsanulirawu ndi waukuru; popeza makolo athu sanasunga mau a
Yehova kucita monga mwa zonse zolembedwa m'bukumu.

Hulida aneneratu za kupasuka kwa Yerusalemu

22Namuka Hilikiya ndi iwo aja adawauza mfumu kwa Hulida
mneneri wamkazi, mkazi wa Salumu mwana wa Tokati, mwana wa
Hasire wosunga zobvala, amene anakhala m'Yerusalemu m'dera
laciwiri, nanena naye mwakuti. 23Ndipo iye ananena nao, Atero
Yehova Mulungu wa Israyeli, Muuze munthuyo anakutumizani kwa
ine, 24Atero Yehova, Taonani, ndifikitsira malo ano ndi anthu okhala
m'mwemo coipa, ndico matemberero onse olembedwa m'buku
adaliwerenga pamaso pa mfumu ya Yuda; 25cifukwa anandisiya
Ine, nafukizira milungu yina, kuti autse mkwiyo wanga ndi nchito
zonse za manja ao; cifukwa cace ukali wanga utsanulidwa pamalo
pano wosazimika. 26Koma kwa mfumu ya Yuda amene
anakutumizani kufunsira kwa Yehova, muzitero kwa iye, Atero
Yehova Mulungu wa Israyeli, Kunena za mau udawamva, 27popeza
mtima wako unali woolowa, ndipo wadzicepetsa pamaso pa
Mulungu, pakumva mau ace otsutsana nao malo ano, ndi okhala
m'mwemo, ndi kudzicepetsa pamaso panga, ndi kung'amba
zobvala zako, ndi kulira pamaso panga; Inenso ndakumvera, ati
Yehova. 28Taona, ndidzakusonkhanitsa ku makolo ako, nudzaikidwa
kumanda kwako mumtendere, ndi maso ako sadzapenya zoipa
zonse ndidzafikitsira malo ano ndi okhala m'mwemo. Ndipo
anambwezera mfumu mau.

Yosiya ndi anthu acitanso pangano ndi Mulungu

29Pamenepo mfumu inatumiza anthu, nisonkhanitsa akulu akulu
onse a Yuda ndi Yerusalemu. 30Nikwera mfumu ku nyumba ya
Yehova ndi amuna onse a m'Yuda, ndi okhala m'Yerusalemu, ndi
ansembe ndi Alevi, ndi anthu onse akuru ndi ang'ono; nawerenga
iye m'makutu mwao mau onse a buku la cipangano adalipeza

m'nyumba ya Yehova. 31Ndipo mfumu inaimirira pokhala pace,
nicita pangano pamaso pa Yehova, kuti adzayenda cotsata Yehova,
ndi kusunga malamulo ace, ndi mboni zace, ndi malemba ace, ndi
mtima wace wonse, ndi moyo wace wonse, kucita mau a
cipangano olembedwa m'bukumu. 32Naimiritsapo onse okhala
m'Yerusalemu ndi m'Benjamini. Ndipo okhala m'Yerusalemu
anacita monga mwa cipangano ca Mulungu, Mulungu wa makolo
ao. 33Yosiya nacotsa zonyansa zonse m'maiko onse okhala a ana a
Israyeli, natumikiritsa onse opezeka m'Israyeli, inde kutumikira
Yehova Mulungu wao. Masiku ace onse iwo sanapambuka
kusamtsata Yehova Mulungu wa makolo ao.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Yosiya acita Paskha ku Yerusalemu

1Pamenepo Yosiya anacitira Yehova Paskha m'Yerusalemu, naphera
Paskha tsiku lakhumi ndi cinai la mwezi woyamba. 2Ndipo anaika
ansembe pa udikiro wao, nawalimbikitsa acite utumiki wa nyumba
ya Yehova. 3Nati kwa Alevi akuphunzitsa Aisrayeli onse, ndiwo
opatulima Yehova, Ikani likasa lopatulika m'nyumba imene Solomo
mwana wa Davide mfumu ya Israyeli anaimanga; silikhalanso
katundu pa mapewa anu; tsopano mutumikire Yehova Mulungu
wanu, ndi anthu ace Israyeli. 4Ndipo mudzikonzere monga mwa
nyumba za makolo anu, m'zigawo zanu, monga umo adalembera
Davide mfumu ya Israyeli, ndi umo adalembera Solomo mwana
wace. 5Ndipo muimirire m'malo opatulika, monga mwa
magawidwe a nyumba za makolo za abale anu ana a anthu, akhale
nalo onse gawo la nyumba ya makolo ya Alevi. 6Ndipo muphere
Paskha, nimudzipatule ndi kukonzera abale anu, kucita monga
mwa mau a Yehova ndi dzanja la Mose. 7Ndipo Yosiya anapatsa
ana a anthu zoweta, ana a nkhosa ndi a mbuzi zikhale zonsezo za
nsembe za Paskha kwa ali yense anali komweko; zinafikira zikwi
makumi atatu, ndi ng'ombe zikwi zitatu, ndizo zotapa pa cuma ca
mfumu. 8Ndi akulu ace anapatsa nsembe yaufulu kwa anthu, kwa
ansembe, ndi kwa Alevi. Hilikiya ndi Zekariya ndi Yehieli, atsogoleri
a m'nyumba ya Mulungu, anapatsa ansembe zoweta zazing'ono
zikwi ziwiri mphambu mazana asanu ndi limodzi, ndi ng'ombe
mazana atatu, zikhale nsembe za Paskha. 9Konaniyanso, ndi
Semaya, ndi Netaneli, abale ace, ndi Hasabiya, ndi Yeyeli, ndi
Yosabadi, akuru a Alevi, ana patsa Alevi zoweta zazing'ono zikwi
zisanu, ndi ng'ombe mazana asanu, zikhale nsembe za
Paskha. 10Momwemo anakonzera kutumikiraku, naima ansembe
pokhala pao, ndi Alevi m'zigawo zao, monga umo adawauzira
mfumu. 11Pamenepo anaphera Paskha; ndi ansembe anawaza
mwazi adaulandira m'manja mwa Alevi amene anasenda
nsembezo. 12Ndipo anacotsapo nsembe zopsereza, kuti azipereke
kwa ana a anthu monga mwa magawidwe a nyumba za makolo;
azipereke kwa Yehova monga mulembedwa m'buku la Mose.
Natero momwemo ndi ng'ombezo. 13Ndipo anaoca Paskha pamoto,
monga mwa ciweruzo; koma zopatulikazo anaziphika m'miphika,
ndi m'mitsuko, ndi m'ziwaya; nazipereka msanga kwa ana onse a
anthu. 14Ndi pambuyo pace anadzikonzera okha ndi ansembe;
popeza ansembe, ana a Aroni, analikupereka nsembe zopsereza
ndi mafuta mpaka usiku; cifukwa cace Alevi anadzikonzera okha
ndi ansembe ana a Aroni. 15Ndi oyimbira, ana a Asafu, anali
pokhala pao, monga adalamulira Davide, ndi Asafu, ndi Hemani,
ndi Yedutuni mlauli wa mfumu; ndi olindirira anali pa zipata zonse,

analibe kuleka utumiki wao; pakuti abale ao Alevi
anawakonzera 16Momwemo kutumikira konse kwa Yehova
kunakonzeka tsiku lomwelo, kucita Paskha, ndi kupereka nsembe
zopsereza pa guwa la nsembe la Yehova, monga analamulira
mfumu Yosiya. 17Ndipo ana a Israyeli okhalako anacita Paskha
nthawi yomweyo, ndi madyerero a mkate wopanda cotupitsa
masiku asanu ndi awiri. 18Panalibe Paskha wocitika m'Israyeli
wonga ameneyu, kuyambira masiku a Samueli mneneri;
panalibenso wina wa mafumu a Israyeli anacita Paskha wotere,
ngati ameneyu anacita Yosiya, ndi ansembe, ndi Alevi, ndi Ayuda
onse, ndi Aisrayeli opezekako, ndi okhala m'Yerusalemu. 19Yosiya
atakhala mfumu zaka khumi ndi zisanu ndi ziwiri anacita Paskha
amene.

Yosiya ayambana ndi Neko mfumu ya Aigupto, naphedwa

20Citatha ici conse, Yosiya atakonza nyumbayi, Neko mfumu ya
Aigupto anakwera kuyambana ku Karikemisi ku Firate; ndipo Yosiya
anamturukira kuyambana naye. 21Koma Neko anatuma mithenga
kwa iye, ndi kuti, Ndiri ndi ciani ndi inu, mfumu ya Yuda?
sindinafika kuyambana ndi inu lero, koma ndi nyumba imene ndiri
nayo nkhondo; ndipo Mulungu anati ndifulumire; lekani kubvutana
ndi Mulungu amene ali nane, Iye angakuonongeni. 22Koma Yosiya
sanatembenuka nkhope yace kumleka, koma anadzizimbaitsa kuti
ayambane naye, osamvera mau a Neko ocokera m'kamwa mwa
Mulungu; nadza kuyambana naye m'cigwa ca Megido. 23Ndipo
oponya anayang'anitsa mibvi pa mfumu Yosiya, niti mfumu kwa
anyamata ace, Ndicotseni ndalasidwa ndithu. 24Pamenepo
anyamata ace anamturutsa m'gareta, namuika m'gareta waciwiri
anali naye, nabwerera naye ku Yerusalemu; nafa iye naikidwa
m'manda a makolo ace. Ayuda onse ndi Yerusalemu nalira
Yosiya. 25Ndipo Yeremiya anamlembera Yosiya nyimbo yomlira; ndi
oyimbira onse, amuna ndi akazi, amanena za Yosiya nyimbo za
maliro zao mpaka lero lino; naziika zikhale lemba m'Israyeli;
taonani, zilembedwa m'Nyimbo za Maliro. 26Macitidwe ena tsono a
Yosiya, ndi nchito zace zokoma, monga mulembedwa m'cilamulo
ca Yehova, 27ndi zocita iye, zoyamba ndi zotsiriza, taonani,
zilembedwa m'buku la mafumu a Israyeli ndi Yuda.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Yehoahazi, Yehoyakimu, Yehoyakini, mafumu a Yuda

1Pamenepo anthu a m'dziko anatenga Yehoahazi mwana wa Yosiya,
namlonga ufumu m'Yerusalemu, m'malo mwa atate
wace. 2Yehoahazi anali wa zaka makumi awiri mphambu zitatu
polowa ufumu wace, nakhala mfumu m'Yerusalemu miyezi
itatu. 3Ndipo mfumu ya Aigupto anamcotsera ufumu wace
m'Yerusalemu, nasonkhetsa dziko matalente zana limodzi a siliva,
ndi talente limodzi la golidi. 4Ndi mfumu ya Aigupto anamlonga
Eliyakimu mng'ono wace mfumu ya Yuda ndi Yerusalemu, nasintha
dzina lace likhale Yehoyakimu. Koma Neko anatenga Yehoahazi
mkuru wace, namuka naye ku Aigupto.
5Yehoyakimu anali wa zaka makumi awiri mphambu zisanu polowa
ufumu wace, nakhala mfumu m'Yerusalemu zaka khumi ndi
cimodzi, nacita coipa pamaso pa Yehova Mulungu
wace. 6Nebukadinezara mfumu ya ku Babulo anakwera
kuyambana naye, nammanga ndi matangadza kumuka naye ku
Babulo. 7Nebukadinezara anatenganso zipangizo za nyumba ya
Yehova kumka nazo ku Babulo, naziika m'kacisi wace ku
Babulo. 8Macitidwe ena tsono a Yehoyakimu, ndi zonyansa zace
anazicita, ndi zija zidapezeka zomtsutsa; taonani, zilembedwa
m'buku la mafumu a Israyeli ndi Yuda; ndi Yehoyakini mwana wace
anakhala mfumu m'malo mwace.
9Yehoyakini anali wa zaka zisanu ndi zitatu polowa ufumu wace,
nakhala mfumu m'Yerusalemu miyezi itatu, ndi masiku khumi;
nacita coipa pamaso pa Yehova. 10Ndipo pofikanso nyengo, mfumu
Nebukadinezara anatumiza anthu abwere naye ku Babulo,
pamodzi ndi zipangizo zokoma za nyumba ya Yehova; nalonga
Zedekiya mbale wace mfumu ya Yuda ndi Yerusalemu.

Zedekiya woipa, mfumu yotsiriza ya Yuda

11Zedekiya anali wa zaka makumi awiri mphambu cimodzi polowa
ufumu wace, nakhala mfumu m'Yerusalemu zaka khumi ndi
cimodzi, 12nacita coipa pamaso pa Yehova Mulungu wace;
sanadzicepetsa kwa Yeremiya mneneri wakunena zocokera
pakamwa pa Yehova. 13Ndiponso anapandukana naye mfumu
Nebukadinezara, amene adamlumbiritsa pa Mulungu; koma
anaumitsa khosi lace, nalimbitsa mtima wace kusatembenukira
kwa Yehova Mulungu wa Israyeli, 14Ndiponso ansembe akulu onse
ndi anthu anacurukitsa zolakwa zao, monga mwa zonyansa zonse
za amitundu, nadetsa nyumba ya Yehova, imene ana patula
m'Yerusalemu. 15Ndipo Yehova Mulungu wa makolo ao anatumiza
kwa iwo, ndi dzanja la mithenga yace, nalawirira mamawa
kuituma, cifukwa anamvera cifundo anthu ace, ndi pokhala
pace; 16koma ananyodola mithenga ya Mulungu, napeputsa mau

ace, naseka aneneri ace, mpaka ukali wa Mulungu unaukira anthu ace, mpaka panalibe colanditsa.

Yerusalemu apasulidwa anthu natengedwa ukapolo ku Babulo

17Pakuti Iye anawakweretsera mfumu ya Akasidi, ndiye
anawaphera anyamata ao ndi lupanga, m'nyumba ya malo ao
opatulika, osacitira cifundo mnyamata kapena namwali, mkulu
kapena nkhalamba; Mulungu anawapereka onse m'dzanja
lace. 18Ndi zipangizo zonse za nyumba ya Mulungu, zazikuru ndi
zazing'ono, ndi cuma ca nyumba ya Yehova, ndi cuma ca mfumu,
ndi ca akalonga ace, anabwera nazo zonsezi ku Babulo. 19Ndipo
anatentha nyumba ya Mulungu, nagumula linga la Yerusalemu,
natentha nyumba zace zonse zacifumu ndi moto, naononga
zipangizo zace zonse zokoma. 20Ndi iwo amene adapulumuka
kulupanga anamuka nao ku Babulo, nakhala iwo anyamata ace,
ndi a ana ace, mpaka mfumu ya Perisiya idacita ufumu; 21kuti
akwaniridwe mau a Yehova pakamwa pa Yeremiya, mpaka dziko
linakondwera nao masabata ace; masiku onse a kupasuka kwace
linasunga sabata, kukwaniritsa zaka makumi asanu ndi awiri.

Koresi alola yense wofuna abwere kwao kukamanga Kacisi

22Caka coyamba tsono ca Koresi mfumu ya Perisiya, kuti
akwaniridwe mau a Yehova pakamwa pa Yeremiya, Yehova anautsa
mzimu wa Koresi mfumu ya Perisiya, kuti abukitse mau m'ufumu
wace wonse, nawalembenso, ndi kuti, 23Atero Koresi mfumu ya
Perisiya, Yehova Mulungu Wam'mwamba anandipatsa maufumu
onse a pa dziko lapansi, nandilangiza ndimmangire nyumba
m'Yerusalemu, ndiwo ku Yuda. Ali yense mwa inu a anthu ace onse,
Yehova Mulungu wace akhale naye, akwereko.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Ana a Israyeli, adzukulu a Yuda

1Ana a Israyeli ndi awa: Rubeni, Simeoni, Levi, ndi Yuda, Isakara,
ndi Zebuluni, 2Dani, Yosefe, ndi Benjamini, Nafitali, Gadi, ndi Aseri.
3Ana a Yuda ndiwo Eri, ndi Onani, ndi Sela; Batisua Mkanani
anambalira atatu amenewa. Koma Eri mwana woyamba wa Yuda
anali woipa pamaso pa Yehova, ndi iye anamupha. 4Ndi Tamari
mpongozi wace anambalira Perezi ndi Zera. Ana amuna onse a
Yuda ndiwo asanu. 5Ana a Perezi: Hezironi, ndi Hamuli. 6Ndi ana a
Zera: Zimri, ndi Etani, ndi Hemani, ndi Kalikoli, ndi Dara; onse
pamodzi ndi asanu. 7Ndi ana a Karmi: Akari wobvuta Israyeliyo,
amene analakwira coperekedwa ciperekereco. 8Ndi mwana wa
Etani: Azariya. 9Ndi ana a Hezironi anambadwirawo: Yerameli, ndi
Ramu, ndi Kelubai. 10Ndi Ramu anabala Aminadabu; ndi
Aminadabu anabala Nasoni kalonga wa ana a Yuda; 11ndi Nasoni
anabala Salima, ndi Salima anabala Boazi, 12ndi Boazi anabala
Obedi, ndi Obedi anabala Jese, 13ndi Jese anabala mwana wace
wamwamuna woyamba Eliabu, ndi Abinadabu waciwiri, ndi Simeya
wacitatu, 14Netaneli wacinai, Radai wacisanu, 15Ozemu wacisanu
ndi cimodzi, Davide wacisanu ndi ciwiri; 16ndi alongo ao ndiwo
Zeruya ndi Abigaili. Ndi ana a Zeruya: Abisai ndi Yoabu, ndi
Asaheli; atatu. 17Ndi Abigaili anabala Amasa; ndi atate wa Amasa
ndiye Yeteri M-ismayeli. 18Ndi Kalebi mwana wa Hezroni anabala
ana ndi Azuba mkazi wace, ndi Yerioti; ndipo ana ace ndiwo Yeseri,
ndi Sobabu, ndi Aridoni. 19Namwalira Azuba, ndi Kalebi
anadzitengera Efrati, amene anambalira Huri. 20Ndi Huri anabala
Uri, ndi Uri anabala Bezaleli. 21Ndipo pambuyo pace Hezroni
analowa kwa mwana wamkazi wa Makiri atate wa Gileadi, amene
anamtenga akhale mkazi wace, pokhala wa zaka makumi asanu
ndi Gmodzi mwamunayo; ndipo mkaziyo anambalira Segubu. 22Ndi
Segubu anabala Yairi, amene anali nayo midzi makumi awiri
mphambu itatu m'dziko la Gileadi. 23Ndi Gesuri ndi Aramu
analanda midzi ya Yairi, pamodzi ndi Kenati ndi miraga yace; ndiyo
midzi makumi asanu ndi limodzi. Iwo onse ndiwo ana a Makiri atate
wa Gileadi. 24Ndipo atafa Hezroni m'Kalebi-Efrata, Abiya mkazi wa
Hezroni anambalira Asini atate wa Tekoa. 25Ndi ana a Yerameli
mwana woyamba wa Hezroni ndiwo: woyamba Ramu, ndi Buna,
ndi Oreni, ndi Ozemu, ndi Ahiya. 26Ndipo Yerameli anali naye mkazi
wina dzina lace ndiye Atara, ndiye mace wa Onamu. 27Ndipo ana a
Ramu mwana woyamba wa Yerameli ndiwo Maazi, ndi Yamini, ndi
Ekeri. 28Ndi ana a Onamu ndiwo Samai, ndi Yada; ndi ana a Samai:
Nadabu, ndi Abisuri. 29Ndipo dzina la mkazi wa Abisuri ndiye
Abihaili; ndipo anambalira Abani, ndi Molidi. 30Ndi ana a Nadabu:
Seledi ndi Apaimu; koma Seledi anamwalira wopanda ana. 31Ndi

mwana wa Apaimu: Isi. Ndi mwana wa Isi: Sesani. Ndi mwana wa Sesani: Alai. 32Ndi ana a Yada mbale wa Samai: Yeteri, ndi Yonatani; namwalira: Yeteri wopanda ana. 33Ndi ana a, Yonatani: Peleti, ndi Zaza. Ndiwo ana a Yerameli. 34Ndipo Sesani analibe ana amuna, koma ana akazi. Ndi Sesani anali naye mnyamata M-aigupto dzina lace ndiye Yara. 35Ndipo Sesani anampatsa Yara mnyamata wace mwana wace wamkazi akhale mkazi wace, ndipo anambalira Atai. 36Ndipo Atai anabala Natani, ndi Natani anabala Zabadi, 37ndi Zabadi anabala Efilali, ndi Efilali anabala Obedi, 38ndi Obedi anabala Yehu, ndi Yehu anabala Azariya, 39ndi Azariya anabala Helezi, ndi Helezi anabala Eleasa, 40ndi Eleasa anabala Sismai, ndi Sismai anabala Salumu, 41ndi Salumu anabala Yekamiya, ndi Yekamiya anabala Elisama. 42Ndi ana a Kalebi mbale wa Yerameli ndiwo Mesa mwana wace woyamba, ndiye atate wa Zifi; ndi ana a Maresa atate wa Hebroni. 43Ndi ana a Hebroni: Kora, ndi Tapuwa, ndi Rekemu, ndi Sema. 44Ndi Sema anabala Rahamu atate wa Yorikeamu, ndi Rekemu anabala Samai. 45Ndi mwana wa Samai ndiye Maoni; ndipo Maoni ndiye atate wa Betizuri. 46Ndi Efa mkazi wamng'ono wa Kalebi anabala Harani, ndi Moza, ndi Gazezi; ndi Harani anabala Gazezi. 47Ndi ana a Yadai: Regemu, ndi Yotamu, ndi Gesam, ndi Peleti, ndi Efa, ndi Safa. 48Maka mkazi wamng'ono wa Kalebi anabala Seberi, ndi Tirana. 49Iyeyu anabalanso Safa atate wa Madimana, Seva atate wa Makibena, ndi atate wa Gibeya; ndi mwana wamkazi wa Kalebi ndiye Akisa. 50Ana a Kalebi ndi awa: mwana wa Huri, mwana woyamba wa Efrata, Sobali atate wa Kiriate Yearimu. 51Salma atate wa Betelehemu, Harefi atate wa Betigaderi. 52Ndipo Sobali atate wa Kiriati-Yearimu anali ndi ana: Haroe, ndi Hazi Hamenukoti. 53Ndi mabanja a Kiriati-Yearimu: Aitiri, ndi Aputi, ndi Asumati, ndi Amisrai; Aforati ndi Aestaoli anafuma kwa iwowa. 54Ana a Salma: Betelehemu, ndi Anetofati, Atroti Beti Yoabu, ndi Hazi Hamanahati, ndi Azori. 55Ndi mabanja a alembi okhala ku Yabezi: Atirati, Asimeati, Asukati. Iwo ndiwo Akeni ofuma ku Hamati, kholo la nyumba ya Rekabu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Adzukulu a Davide

1Ana Davide tsono ombadwira ku Hebroni: woyamba a Amnoni wa
Ahinoamu wa ku Yezreeli, waciwiri Danieli wa Abigaili wa ku
Karimeli, 2wacitatu Abisalomu mwana wa Maaka mwana wamkazi
wa Talimai mfumu ya Gesuri, wacinai Adoniya mwana wa
Hagiti, 3wacisanu Sefatiya wa Abitali, wacisanu ndi cimodzi
Itreamu wa mkazi wace Egila, 4Anambadwira asanu ndi mmodzi
m'Hebroni; ndi pomwepo anakhala mfumu zaka zisanu ndi ziwiri,
ndi miyezi isanu ndi iwiri; ndi m'Yerusalemu anakhala mfumu zaka
makumi atatu mphambu zitatu. 5Ndipo ombadwira m'Yerusalemu
ndi awa: Simeya, ndi Sobabu, ndi Natani, ndi Solomo, anai a
Batisuwa mwana wamkazi wa Amieli; 6ndi Ibara, ndi Elisama, ndi
Elifeleti, 7ndi Noga, ndi Nefegi, ndi Yafiya, 8ndi Elisama, ndi Eliada,
ndi Elifeleti, asanu ndi anai. 9Onsewa ndiwo ana a Davide, pamodzi
ndi ana a akazi ang'ono; ndipo Tamara ndiye mlongo wao. 10Ndipo
mwana wa Solomo ndiye Rehabiamu, Abiya mwana wace, Asa
mwana wace, Yeo hosafati mwana wace, 11Yoramu mwana wace,
Ahaziya mwana wace, Yoasi mwana wace, 12Amaziya mwana
wace, Azariya mwana wace, Yotamu mwana wace, 13Ahazi mwana
wace, Hezekiya mwana wace, Manase mwana wace, 14Amoni
mwana wace, Yosiya mwana wace. 15Ndi ana a Yosiya: woyamba
Yohanana, waciwiri Yehoyakimu, wacitatu Zedekiya, wacinai
Salumu. 16Ndi ana a Yehoyakimu: Yekoniya mwana wace, Zedekiya
mwana wace. 17Ndi mwana wa Yekoniya: Asiri, Sealitiyeli mwana
wace, 18ndi Malikiramu, ndi Pedaya, ndi Senazara, Yekamiya,
Hosama, Nedabiya. 19Ndi ana a Pedaya: Zerubabeli, ndi Simei; ndi
ana a Zerubabeli: Mesulamu, ndi Hananiya; ndipo Selomiti ndiye
mlongo wao, 20ndi Hasuba, ndi Oheli, ndi Berekiya, ndi Hasadiya,
ndi Yusabi-hesedi; asanu. 21Ndi ana a Hananiya: Pelatiya, ndi
Yesaya, ana a Refaya, ana a Arinani, ana a Obadiya, ana a
Sekaniya. 22Ndi mwana wa Sekaniya: Semaya; ndi ana a Semaya:
Hatusi, ndi Igali, ndi Bariya, ndi Neariya, ndi Safati; asanu ndi
mmodzi. 23Ndi ana a Neariya: Eliunai, ndi Hizikiya, ndi Azrikamu,
atatu. 24Ndi ana a Eliunai: Hodavia, ndi Eliasibu, ndi Pelaya, ndi
Akubu, ndi Yohanana, ndi Delaya, ndi Anani, asanu ndi awiri.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Adzukulu a Yuda

1Ana a Yuda: Perezi, Hezroni, ndi Karmi, ndi Huri, ndi
Sobala. 2Ndipo Reaya mwana wa Sobala anabala Yahati; ndi Yahati
anabala Ahumai, ndi Lahadi. Iwo ndiwo mabanja a Azorati. 3Iwo
ndiwo a atate wa Etamu: Yezreeli, ndi Isma, ndi Idibasi; ndipo dzina
la mlongo wao ndiye Hazeleleponi, 4ndi Penueli atate wa Gedoro,
ndi Ezeri atate wa Husa. Awa ndi ana a Huri woyamba wa Efrata
atate wa Betelehemu. 5Ndipo Asuri atate wa Tekowa anali nao
akazi awiri: Hela, ndi Naara. 6Ndi Naara anambalira Ahuzamu, ndi
Heferi, ndi Temeni, ndi Hahastario Iwo ndiwo ana a Naara. 7Ndi ana
a Hela ndiwo Zereti, Izara, ndi Etinani. 8Ndipo Hakozi anabala
Anubu, ndi Zobeba, ndi mabanja a Ahareli mwana wa
Harumu. 9Ndipo Yabezi analemekezedwa koposa abale ace; ndi
mace anamucha dzina lace Yabezi, ndi kuti, Popeza ndambala
mwaululu. 10Ndipo Yabezi anaitana kwa Mulungu wa Israyeli, ndi
kuti, Mundidalitse ndithu, ndi kukulitsa malire anga; ndi dzanja
lanu likhale ndi ine, nimundisunge, kuti coipa cisandibvute. Ndipo
Mulungu anafikitsa copempha iye. 11Ndipo Kelubu mbale wa Sua
anabala Mehiri, ndiye atate wa Esitoni. 12Ndi Esitoni anabala
Betirafa, ndi Paseya, ndi Tehina atate wa Irinahasi. Awa ndi anthu a
Reka. 13Ndi ana a Kenazi: Otiniyeli, ndi Seraya; ndi mwana wa
Otmiyeh: Hatati. 14Ndipo Meonotai anabala Ofra; ndi Seraya
anabala Yoabu atate wa Geharasimu; popeza iwo ndiwo
amisiri. 15Ndi ana a Kalebi mwana wa Yefune: Iru, Ela, ndi Naamu;
ndi ana a Ela, ndi Kenazi. 16Ndi ana a Yehaleleli: Ziti, ndi Zifa,
Tiriya, ndi Asareli. 17Ndi ana a Ezra: Yeteri, ndi Meredi, ndi Eferi, ndi
Yaloni; ndipo anabala Miriamu, ndi Samai, ndi Isba atate wa
Esitemowa. 18Ndi mkazi wace Myuda anabala Yeredi atate wa
Gedoro, ndi Heberi atate wa Soko, ndi Yekutiyeli atate wa Zanowa.
Ndipo awa ndi ana a Bitiya mwana wamkazi wa Farao, amene
Meredi anamtenga. 19Ndi ana a mkazi wa Hodiya, mlongo wace wa
Nahamu, ndiwo atate a Kula Mgarimi ndi Esitemowa
Mmaaka. 20Ndi ana a Simoni; Amnoni, ndi Rina, Benehanana, ndi
Tiloni. Ndi ana a Isi: Zoheti, ndi Benzoheti. 21Ana a Sela mwana wa
Yuda: Eri atate wa Leka, ndi Laada atate wa Maresa, ndi mabanja a
nyumba ya iwo oomba bafuta wa thonje losansitsa a nyumba ya
Asibeya, 22ndi Yokimu, ndi amuna a Kozeba, ndi Yoasi, ndi Sarafa
wolamulira m'Moabu, ndi Yasubilehemu; koma mau awa ndiwo a
kale lomwe. 23Iwo ndiwo oumba mbiya, ndi okhala m'Netaimu, ndi
m'Gedera; anakhala komweko ndi mfumu m'nchito yace.

Adzukulu a Simeoni

24Ana a Simeoni: Nemueli, ndi Yamini, Yaribi, Zera, Sauli, 25Salumu
mwana wace, Mibsamu mwana wace, Misma mwana wace. 26Ndi

ana a Misma: Hamueli mwana wace, Zakuri mwana wace, Simei mwana wace. 27Ndipo Simei anali nao ana amuna khumi mphambu asanu ndi mmodzi, ndi ana akazi asanu ndi mmodzi; koma abale ace analibe ana ambiri, ndi banja lao lonse silinacurukitsa ngati ana a Yuda. 28Ndipo anakhala ku Beereseba, ndi Molada, ndi Hazarasuala, 29ndi ku Bila, ndi ku Ezemu, ndi ku Toladi, 30ndi ku Betueli, ndi ku Horima, ndi ku Zikilaga, 31ndi ku Betimarikaboti, ndi ku Hazarasusimu, ndi ku Betibiri, ndi ku Saraimu. Iyi ndi midzi yao, mpaka ufumu wa Davide, pamodzi ndi miraga yao. 32Etamu, ndi Aini, Rimoni, ndi Tokeni, ndi Asani, midzi isanu; 33ndi miraga yao yonse pozungulira pace pa midzi yomweyi, mpaka Baala. Apo ndi pokhala pao ndipo ali nao mawerengedwe a maina ao. 34Ndi Mesobabu, ndi Yamleki, ndi Yosa mwana wa Amaziya, 35ndi Yoeli, ndi Yehu mwana wa Yosibiya, mwana wa Seraya, mwana wa Asieli; 36ndi Eliunai, ndi Yaakoba, ndi Yesohaya, ndi Asaya, ndi Adieli, ndi Yesimieli, ndi Benaya, 37ndi Ziza mwana wa Sifi, mwana wa Aloni, mwana wa Yedaya, mwana wa Simri, mwana wa Semaya; 38awa ochedwa maina ndiwo akalonga m'mabanja ao, ndi nyumba za makolo ao zinacuruka kwambiri. 39Ndipo anamuka mpaka polowera ku Gedoro kum'mawa kwa cigwa, kufunafuna podyetsa zoweta zao. 40Ndipo anapeza podyetsa ponenepetsa ndi pabwino, ndipo dzikoli ndi lacitando ndi lndikha ndi losungikamo, pakuti okhalako kale ndiwo a Hamu. 41Iwo tsono olembedwa maina anadza masiku a Hezekiya mfumu ya Yuda, nakantha mahema ao ndi zokhalamo zao, naziononga konse mpaka lero, nakhala m'malo mwao; popeza panali podyetsa zoweta zao pamenepo. 42Ndipo ena a iwowa a ana a Simeoni, amuna mazana asanu, anamka ku phiri la Seiri; akuwatsogolera ndiwo Pelatiya, ndi Neariya, ndi Refaya, ndi Uzieli; ana a lsi. 43Nakantha otsala a Aamaleki adapulumukawo, nakhala komweko mpaka lero lino.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Adzukulu a Rubeni

1Ndipo ana a Rubeni mwana woyamba wa Israyeli, (pakuti ndiye
mwana woyamba; koma popeza anaipsa kama wa atate wace
ukulu wace unapatsidwa kwa ana a Yosefe mwana wa Israyeli,
koma m'buku la cibadwidwe asayesedwe monga mwa ukulu
wace. 2Pakuti Yuda anakula mphamvu mwa abale ace, ndi
mtsogoleri anafuma kwa iyeyu, koma ukulu ngwa Yosefe); 3ana a
Rubeni mwana woyamba wa Israyeli: Hanoki, ndi Palu, Hezroni, ndi
Karmi. 4Ana a Yoeli: Semaya mwana wace, Gogi mwana wace,
Simei mwana wace, 5Mika mwana wace, Reaya mwana wace,
Baala mwana wace, 6Beera mwana wace, amene Tigilati Pilesere
wa ku Asuri anamtenga ndende; ndiye kalonga wa Arubeni. 7Ndi
abale ace monga mwa mabanja ao, powerenga cibadwidwe ca
mibadwo yao: akuru ndiwo Yeyeli, ndi Zekariya, 8ndi Bela mwana
wa Azazi, mwana wa Sema, mwana wa Yoeli, wokhala ku Aroeri,
ndi kufikira ku Nebo ndi Baala-meoni; 9ndi kum'mawa anakhala
mpaka polowera kucipululu kuyambira mtsinje wa Firate; pakuti
zoweta zao zinacuruka m'dziko la Gileadi. 10Ndipo masiku a Sauli
anagwirana nkhondo ndi Ahagiri, amene adagwa ndi dzanja lao;
ndipo anakhala m'mahema mwao kum'mawa konse kwa Gileadi.

Adzukulu a Gadi

11Ndi ana a Gadi anakhala pandunji pao m'dziko la Basana mpaka
Saleka: 12Yoeli mkuru wao, ndi Safamu waciwiri, ndi Yanai, ndi
Safati m'Basana; 13ndi abale ao a; nyumba za makolo ao: Mikaeli,
ndi Mesulamu, ndi Seba, ndi Yorai, ndi Yakani, ndi Ziya, ndi Eberi;
asanu ndi awiri. 14Awa ndi ana a Abihaili, mwana wa Huri, mwana
wa Yarowa, mwana wa Gileadi, mwana wa Mikaeli, mwana wa
Yesisai, mwana wa Yado, mwana wa Buzi, 15Ahi mwana wa Abdieli,
mwana wa Guni, ndiye mkulu wa nyumba za makolo ao. 16Ndipo
anakhala m'Gileadi m'Basana, ndi m'midzi yace, ndi podyetsa pace
ponse pa Saroni, mpaka malire ao. 17Onsewo anawerengedwa
monga mwa mabuku a cibadwidwe cao, masiku a Yotamu mfumu
ya Yuda, ndi m'masiku a Yerobiamu mfumu ya Israyeli.
18Ana a Rubeni, ndi a Gadi, ndi limodzi la magawo awiri a pfuko la
Manase, ngwazi, amuna akugwira cikopa ndi lupanga, ndi kuponya
mibvi, ozerewera nkhondo, ndiwo zikwi makumi anai mphambu
zinai mphambu mazana asanu ndi awiri kudza makumi asanu ndi
limodzi akuturuka kunkhondo. 19Ndipo anagwirana nkhondo ndi
Ahagari, ndi Yet uri, ndi Nafisi, ndi Nodabu. 20Ndipo
anathandizidwa polimbana nao; ndi Ahagari anaperekedwa
m'dzanja lao, ndi onse anali nao; pakuti anapfuulira kwa Mulungu
pomenyana nao, ndipo anapembedzeka nao, popeza
anamkhulupirira iye. 21Ndipo analanda zoweta zao, ngamila zao

zikwi makumi asanu, ndi nkhosa zikwi mazana awiri ndi makumi asanu, ndi aburu zikwi ziwiri, ndi amuna zikwi zana limodzi. 22Pakuti adagwa, nafa ambiri, popeza nkhondoyi nja Mulungu. Ndipo anakhala m'malo mwao mpaka anatengedwa ndende.

Adzukulu a Manase kum'mawa

23Ndi ana a limodzi la magawo awiri a pfuko la Manase anakhala m'dziko; anacuruka kuyambira Basana kufikira Baala Herimoni, ndi Seniri, ndi phiri la Herimoni. 24Ndipo akuru a nyumba za makolo ao ndi awa: Eferi, ndi Isi, ndi Elieli, ndi Azrieli, ndi Yeremiya, ndi Hodaviya, ndi Yadieli, anthu amphamvu ndithu, anthu omveka, akulu a nyumba za makolo ao. 25Koma analakwira Mulungu wa makolo ao, nacita cigololo, ndi kutsata milungu ya mitundu ya anthu a m'dziko, amene Mulungu adaononga pamaso pao. 26Ndipo Mulungu wa Israyeli anautsa mzimu wa Puli mfumu ya Asuri, ndi mzimu wa Tigilati Pilesere mfumu ya Asuri, ndiye anawatenga ndende; ndiwo Arubeni, ndi Agadi, ndi pfuko la Manase logawika pakati, nafika nao ku Hala, ndi Habori, ndi Hara ndi ku mtsinje wa Gozani, mpaka lero lino.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Adzukulu a Levi

1Ana a Levi: Gerisomu, Kohati, ndi Merari. 2Ndi ana a Kohati:
Amramu, Izara, ndi Hebroni, ndi Uzieli. 3Ndi ana a Amramu: Aroni,
ndi Mose, ndi Miriamu. Ndi ana a Aroni: Nadabu, ndi Abihu,
Eleazara, ndi Itamara. 4Eleazara anabala Pinehasi, Pinehasi
anabala Abisua, 5ndi Abisua anabala Buki, ndi Buki anabala
Uzi, 6ndi Uzi anabala Zerahiya, ndi Zerahiya anabala
Merayoti, 7Merayoti anabala Amariya, ndi Amariya anabala
Ahitubu, 8ndi Ahitubu anabala Zadoki, ndi Zadoki anabala
Ahimaazi, 9ndi Ahimaazi anabala Azariya, ndi Azariya anabala
Yohanani, 10ndi Yohanani anabala Azariya (ndiye amene anacita
nchito ya nsembe m'nyumba anaimanga Solomo
m'Yerusalemu), 11ndi Azariya anabala Amariya, ndi Amariya
anabala Ahitubu, 12ndi Ahitubu anabala Zadoki, ndi Zadoki anabala
Salumu, 13ndi Salumu anabala Hilikiya, ndi Hilikiya anabala
Azariya, 14ndi Azariya anabala Seraya, ndi Seraya anabala
Yehozadaki, 15ndi Yehozadaki analowa undende muja Yehova
anatenga ndende Yuda ndi Yerusalemu ndi dzanja la
Nebukadinezara.
16Ana a Levi: Gerisomu, Kohati ndi Merari. 17Ndipo maina a ana a
Gerisomu ndi awa: Libni, ndi Simei. 18Ndipo ana a Kohati ndiwo
Amramu, ndi lzara, ndi Hebroni, ndi Uzieli. 19Ana a Merari: Mali ndi
Musi. Ndi mabanja a Alevi monga mwa nyumba za makolo ao ndi
awa. 20Wa Gerisomu: Libni mwana wace, Yahati mwana wace, Zina
mwana wace, 21Yowa mwana wace, Ido mwana wace, Zera mwana
wace, Yeaterai mwana wace. 22Ana a Kohati: Aminadabu mwana
wace, Kora mwana wace, Asiri mwana wace, 23Elikana mwana
wace, ndi Ebiasafu mwana wace, ndi Asiri mwana wace, 24Tahati
mwana wace, Urieli mwana ware, Uziya mwana wace, ndi Sauli
mwana wace. 25Ndi ana a Elikana: Amasai, ndi Ahimoti. 26Elikana:
ana a Elikana Zofai mwana wace, ndi Nahati mwana wace, 27Eliabu
mwana wace, Yerohamu mwana wace, Elikana mwana wace. 28Ndi
ana a Samueli: woyamba Yoeli, ndi waciwiri Abiya. 29Ana a Merari:
Mali, Libni mwana wace, Simei mwana wace, Uza mwana
wace, 30Simeya mwana wace, Hagiya mwana wace, Asaya mwana
wace.

A udindo wa kuyimba

31Ndipo iwo aja Davide anawaimika a udindo wa nyimbo
m'nyumba ya Yehova, litafikira kupumula likasalo, ndi awa. 32Ndipo
anatumikira ndi kuyimba pakhomo pa kacisi wa cihema
cokomanako mpaka Solomo adamanga nyumba ya Yehova
m'Yerusalemu, naimirira m'utumiki wao monga mwa
malongosoledwe ao. 33Ndipo oimirirawo, ndi ana ao, ndi awa: a

ana a Akohati, Hemani woyimbayo, mwana wa Yoeli, mwana wa Samueli, 34mwana wa Elikana, mwana wa Yerohamu, mwana wa Elieli, mwana wa Towa, 35mwana wa Zufi, mwana wa Elikana, mwana wa Mahati, mwana wa Amasai, 36mwana wa Elikana, mwana wa Yoeli, mwana wa Azariya, mwana wa Zefaniya, 37mwana wa Tahati, mwana wa Asiri, mwana wa Abiasafu, mwana wa Kora, 38mwana wa Izara, mwana wa Kohati, mwana wa Levi, mwana wa Israyeli. 39Ndi mbale wace Asafu wokhala ku dzanja lace lamanja, ndiye Asafu mwana wa Berekiya, mwana wa Simeya, 40mwana wa Mikaeli, mwana wa Baaseya, mwana wa Malikiya, 41mwana wa Etini, mwana wa Zera, mwana wa Adaya, 42mwana wal Edani, mwana wa Zima, mwana wa Simeyi, 43mwana wa Yabati, mwana wa Gerisomu, mwana wa Levi. 44Ndi ku dzanja lamanzere abale ao ana a Merari: Etani mwana wa Kisi, mwana wa Abidi, mwana wa Maluki, 45mwana wa Hasabiya, mwana wa Amaziya, mwana wa Hilikiya, 46mwana wa Amzi, mwana wa Bani, mwana wa Semeri, 47mwana wa Mali, mwana wa Musi, mwana wa Merari, mwana wa Levi. 48Ndi abale ao Alevi anaikidwa acite za utumiki ziti zonse za kacisi wa nyumba ya Mulungu.

Ansembe mwa Alevi

49Koma Aroni ndi ana ace adafofukiza pa guwa la nsembe yopsereza, ndi pa guwa la nsembe yofukiza, cifukwa ca nchito yonse ya malo opatulikitsa, ndi kucitira Israyeli cowatetezera, monga mwa zonse Mose mtumiki wa Mulungu adawauza. 50Ndipo ana a Aroni ndiwo Eleazara mwana wace, Pinehasi mwana wace, Abisua mwana wace, 51Buki mwana wace, Uzi mwana wace, Zerobiya mwana wace, 52Merayoti mwana wace, Amariya mwana wace, Ahitubu mwana wace, 53Zadoki mwana wace, Ahimaazi mwana wace.

Midzi va Alevi

54Pokhala pao tsono monga mwa madera ao m'malire mwao ndi awa: kwa ana a Aroni a mabanja a Akobati, pakuti maere oyamba adagwera iwowa, 55kwa iwo anapereka Hebroni m'dziko la Yuda, ndi podyetsa pace pozungulira pace; 56koma minda ya mudzi ndi miraga yace anapatsa Kalebi mwana wa Yefune. 57Ndi kwa ana a Aroni anapereka midzi yopulumukirako: Hebroni, ndi Libina ndi mabusa ace, ndi Yatiri, ndi Esitemowa ndi mabusa ace, 58ndi Hileni ndi mabusa ace, ndi Debiri ndi mabusa ace, 59ndi Asani ndi mabusa ace, ndi Betesemesi ndi mabusa ace; 60ndi ku pfuko la Benjamini Geba ndi mabusa ace, ndi Alemeti ndi mabusa ace, ndi Anatoti ndi mabusa ace. Midzi yao yonse mwa mabanja ao ndiyo midzi khumi ndi itatu. 61Ndipo otsala a ana a Kohati analandira mwa maere, motapa pa mabanja a pfuko, pa pfuko la Manase

logawika pakati, midzi khumi. 62Ndi kwa ana a Gerisomu monga
mwa mabanja ao, motapa pa pfuko la Isakara, ndi pa pfuko la
Aseri, ndi pa pfuko la Nafitali, ndi pa pfuko la Manase m'Basana,
midzi khumi ndi itatu. 63Ana a Merari analandira mwa maere
monga mwa mabanja ao, motapa pa pfuko la Rubeni, ndi pa pfuko
la Gadi, ndi pa pfuko la Zebuluni, midzi khumi ndi iwiri. 64Ndipo
ana a Israyeli anapatsa Alevi midzi ndi mabusa ao. 65Ndipo
anapatsa mwamaere, motapa pa pfuko la ana a Yuda, ndi pa pfuko
la Simeoni, ndi pa pfuko la ana a Benjamini, midzi iyi yochulidwa
maina ao. 66Ndi mabanja ena a ana a Kohati anali nayo midzi ya
malire ao, yotapa pa pfuko la Efraimu. 67Ndipo anawapatsa midzi
yopulumukiramo: Sekemu ndi mabusa ace ku mapiri a Efraimu,
Gezeri ndi mabusa ace, 68ndi Yokimeamu ndi mabusa ace, ndi
Betihoroni ndi mabusa ace, 69ndi Ayaloni ndi mabusa ace, ndi
Gatirimoni ndi mabusa ace, 70ndi motapa pa pfuko la Manase
logawika pakati, Aneri ndi mabusa ace, ndi Bileamu ndi mabusa
ace, kwa otsala a mabanja a ana a Kohati. 71Ana a Gerisomu
analandira motapa pa mabanja a pfuko la Manase logawika pakati,
Golani m'Basana ndi mabusa ace, ndi Asitaroti ndi mabusa
ace; 72ndi motapa pa pfuko la Isakara, Kedesi ndi mabusa ace,
Daberati ndi mabusa ace, 73ndi Ramoti ndi mabusa ace, ndi
Anemu ndi mabusa ace; 74ndi motapa pa pfuko la Aseri, Masala ndi
mabusa ace, ndi Abidoni ndi mabusa ace, 75ndi Hukoki ndi mabusa
ace, ndi Rehobu ndi mabusa ace; 76ndi motapa pa pfuko la Nafitali,
Kadesi m'Galileya ndi mabusa ace, ndi Hamoni ndi mabusa ace,
ndi Kiriyataimu ndi mabusa ace. 77Otsala a Alevi analandira,
motapa pa pfuko la Zebuluni, Rimono ndi mabusa ace, Tabora ndi
mabusa ace; 78ndi tsidya lija la Yordano kum'mawa kwa Yordano
analandira, motapa pa pfuko la Rubeni, Bezeri m'cipululu ndi
mabusa ace, ndi Yaza ndi mabusa ace, 79ndi Kedemoti ndi mabusa
ace, ndi Mefati ndi mabusa ace; 80ndi motapa m'pfuko la Gadi,
Ramoti m'Gileadi ndi mabusa ace, ndi Mahanaimu ndi mabusa
ace, 81ndi Hezboni ndi mabusa ace, ndi Yazeri ndi mabusa ace.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Adzukulu a Isakara

1Ana a Isakara ndiwo Tola, ndi Pua, Yasubu ndi Simironi; anai. 2Ndi
ana a Tola: Uzi, ndi Repaya, ndi Yerieli, ndi Yamai, ndi Ibsamu, ndi
Semueli, akuru a nyumba za makolo; ao ndiwo a Tola, ngwazi
zamphamvu, m'mibadwo yao; kuwerenga kwao masiku a Davide
ndiko zikwi makumi awiri mphambu ziwiri kudza mazana asanu ndi
limodzi. 3Ndi mwana wa Uzi: Izrahiya; ndi ana a Izrahiya: Mikaeli,
ndi Obadiya, ndi Yoeli, ndi Isiya; onse asanuwa ndiwo akuru. 4Ndi
pamodzi nao mwa mibadwo yao, mwa nyumba za makolo ao,
panali magulu a nkhondo zikwi makumi atatu mphambu zisanu ndi
cimodzi, popeza anacuruka akazi ao ndi ana ao. 5Ndi abale ao mwa
mabanja onse a Isakara, ngwazi zamphamvu, oyesedwa mwa
cibadwidwe cao, onsewa ndiwo zikwi zisanu ndi zitatu mphambu
zisanu ndi ziwiri.

Adzukulu a Benjamini ndi Nafitali

6Ana a Benjamini ndiwo Bela, ndi Bekeri, ndi Yedyaeli, atatu. 7Ndi
ana a Bela: Ezboni, ndi Uzi, ndi Uzieli, ndi Yerimoti, ndi hi, asanu;
akuru a nyumba za makolo ao, ngwazi zamphamvu, owerengedwa
m'mabuku a cibadwidwe zikwi makumi awiri mphambu ziwiri kudza
makumi atatu ndi anai. 8Ndi ana a Bekeri: Zemira, ndi Yoasi, ndi
Eliezeri, ndi Eliunai, ndi Omri, ndi Yeremoti, ndi Abiya, ndi Anatoti,
ndi Alemeti. Onsewa ndiwo ana a Bekeri. 9Ndipo anayesedwa mwa
cibadwidwe cao, mwa mibadwo yao, akulu a nyumba za makolo
ao, ngwazi zamphamvu zikwi makumi awiri mphambu mazana
awiri. 10Ndi mwana wa Yedyaeli: Bilani; ndi ana a Bilani: Yeusi, ndi
Benjamini, ndi Ehudi, ndi Kenana, ndi Zetani, ndi Tarasisi, ndi
Ahisabara. 11Onsewa ndiwo ana a Yedyaeli; ndiwo akuru a nyumba
za makolo ao, ngwazi zamphamvu zikwi khumi mphambu zisanu
ndi ziwiri kudza mazana awiri akuturuka kugulu
kunkhondo. 12Sufimu yemwe ndi Hupimu ana a Iri, ndi Husimu
mwana wa Aheri.

13Ana a Nafuali: Yazieli, ndi Guni, ndi Yezeri, ndi Salumu, ana a Bila.

Adzukulu a Manase

14Ana a Manase ndiwo Asrieli amene mkazi wace anambala, Koma
mkazi wace wamng'ono Maramu anabala Makiri atate wa
Gileadi; 15ndi Makiri anadzitengera mkazi, mlongo wace wa
Hupimu ndi Supimu, dzina lace ndiye Maaka. Ndipo dzina la
mwana waciwiri wa Manase ndiye Tselofekadi. Ndi Tselofekadi anali
ndi ana akazi. 16Ndi Maaka mkazi wa Makiri anabala mwana,
namucha dzina lace Peresi, ndi dzina la mbale wace ndiye Seresi,
ndi ana ace ndiwo Ulamu, ndi Rakemu. 17Ndi mwana wa Ulamu:
Bedani; ndiwo ana a Gileadi mwana wa Makiri mwana wa
Manase. 18Ndi mlongo wace Hamoleketi anabala Isodi, ndi

Abiezeri, ndi Mala. 19Ndi ana a Semida ndiwo Ahiani, ndi Sekemu, ndi Liki, ndi Aniamu.

A Efraimu

20Ndi ana a Efraimu: Sutera, ndi Beredi mwana wace, ndi Tahati mwana wace, ndi Ekada mwana wace, ndi Tahati mwana wace, 21ndi Zabadi mwana wace, ndi Sutela mwana wace, ndi Ezeri, ndi Eleadi, amene anthu a Gadi obadwa m'dziko anamupha, popeza anatsikira kukalanda zoweta zao. 22Ndipo Efraimu atate wao, anacita maliro masiku ambiri, ndi abale ace anadza kudzamtonthoza mtima. 23Ndipo analowa kwa mkazi wace, naima iye, nabala mwana, namucha dzina lace Beriya, popeza m'nyumba mwace mudaipa. 24Ndipo mwana wace wamkazi ndiye Seera, amene anamanga Beti-horoni wa kunsi, ndi Beti-horoni wa kumtunda, ndi Uzeniseera. 25Ndipo Refa anali mwana wace, ndi Resefe, ndi Tela mwana wace, ndi Tahani mwana wace, 26Ladana mwana wace, Amihudi mwana wace, Elisamu mwana wace, 27Nuni mwana wace, Yoswa mwana wace. 28Ndipo dziko lao, ndi pokhala pao ndizo Beteli ndi miraga yace, ndi kum'mawa Narani, ndi kumadzulo Gezeri ndi miraga yace, ndi Sekemu ndi miraga yace, mpaka Aza ndi miraga yace; 29ndi kumalire a ana a Manase; Beteseani ndi miraga yace, Taanaki ndi miraga yace, Megido ndi miraga yace, Dora ndi miraga yace. M'menemo anakhala ana a Yosefe mwana wa Israyeli.

30Ana a Aseri: Imna, ndi Isva, ndi Isvi, ndi Beriya, ndi Sera mlongo wao. 31Ndi ana a Beriya: Heberi, ndi Malikieli, ndiye atate wa Birizaiti. 32Ndi Heberi anabala Yafteti, ndi Someri, ndi Hotamu, ndi Suwa mlongo wao. 33Ndi ana a Yafteti: Pasaki, ndi Bimali, ndi Asvati. Awa ndi ana a Yafteti. 34Ndi ana a Semeri: Ahi, ndi Roga, Yehuba, ndi Aramu. 35Ndi ana a Helemu mbale wace: Zofa, ndi Imna, ndi Selesi, ndi Amali. 36Ana a Zofa: Suwa, ndi Harineferi, ndi Sauli, ndi Beri, ndi Imra, 37Bezeri, ndi Hndi, ndi Sama, ndi Silisa, ndi Itirani, ndi Beera. 38Ndi ana a Yeteri: Yefune, ndi Pisipa, ndi Ara. 39Ndi ana a Ula: Ara, ndi Hanieli, ndi Rizya. 40Awa onse ndiwo ana a Aseri, akuru a nyumba za makolo ao, ngwazi zosankhika ndi zamphamvu, akuru mwa akalonga. Oyesedwa mwa cibadwidwe cao otumikira kunkhondo ndiwo amuna zikwi makumi awiri mphambu zisanu ndi cimodzi.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Adzukulu a Benjamini ndi Sauli

1Ndipo Benjamini anabala Bela mwana wace vyoyamba, Asibeli
waciwiri, ndi Ahara wacitatu, 2Noha wacinai, ndi Rafa
wacisanu. 3Ndi Bela anali ndi ana: Adara, ndi Gera, ndi
Abihudi, 4ndi Abisuwa, ndi Namani, ndi Ahowa, 5ndi Gera, ndi
Sefufani, ndi Huramu. 6Ndi ana a Ehudi ndi awa: ndiwo akuru a
nyumba za makolo ao a iwo okhala ku Geba, ndipo anawatenga
ndende kumka ku Manahati, 7natenga ndende Namani, ndi Ahiya,
ndi Gera, ndipo, anabala Uza, ndi Ahihudi. 8Ndipo Saharaimu
anabala ana ku dziko la Moabu, atacotsa akazi ace Husimu ndi
Baara. 9Ndipo Hodesi mkazi wace anambalira Yohabu, ndi Zibiya,
ndi Mesa, ndi Malikamu, 10ndi Yeuzi, ndi Sakiya, ndi Mirima. Awa
ndi ana ace akurua nyumbazamakolo ao. 11Ndi Husimu anambalira
Abitubu, ndi Elipaala. 12Ndi ana a Elipaala: Eberi, ndi Misamu, ndi
Semedi, amene anamanga Ono, ndi Ludi ndi miraga yace, 13ndi
Beriya, ndi Sema; ndiwo akuru a nyumba za makolo a iwo okhala
m'Ayaloni, amene anathawitsa okhala m'Gati; 14ndi Ahio, Sasaki,
ndi Yeremoti, 15ndi Zebadiya, ndi Aradi, ndi Ederi, 16ndi Mikaeli, ndi
Isipa, ndi Yoha, ana a Beriya; 17ndi Zebadiya, ndi Mesulamu, ndi
Hiziki, ndi Heberi, 18ndi Ismerai, ndi Izliya, ndi Yobabu, ana a
Elipaala; 19ndi Yakimu, ndi Zikiri, ndi Zabidi, 20ndi Elianai, ndi
Ziletai, ndi Elieli, 21ndi Adaya, ndi Beraya, ndi Simirati, ana a
Simei; 22ndi Isipani, ndi Eberi, ndi Elieli, 23ndi Abidoni, ndi Zikiri, ndi
Hanani, 24ndi Hananiya, ndi Elamu, ndi Antotiya, 25ndi Ifideya, ndi
Penueli, ana a Sasaki; 26ndi Samserai, ndi Sehariya, ndi
Ataliya, 27ndi Yaaresiya ndi Eliya, ndi Zikiri, ana a Yerohamu. 28Awa
ndi akuru a nyumba za makolo mwa mibadwo yao, ndiwo akuru
anakhala m'Yerusalemu awa. 29Ndipo m'Gibeoni anakhala atate a
Gibeoni, dzina la mkazi wace ndiye Maaka; 30ndi mwana wace
woyamba ndiye Abidoni, opondana naye ndi Zuri, ndi Kisi, ndi
Baala, ndi Nadabu, 31ndi Gedoro, ndi Ahiyo, ndi Zekeri. 32Ndipo
Mikiloti anabala Simeya. Ndi iwonso anakhala pamodzi ndi abale
ao m'Yerusalemu, popenyana ndi abale ao. 33Ndipo Neri anabala
Kisi, ndi Kisi anabala Sauli, ndi Sauli anabala Yonatani, ndi
Malikisuwa, ndi Abinadabu, ndi Esibaala. 34Ndi mwana wa Yonatani
ndiye Meri-baala; ndi Meri-baala anabala Mika. 35Ndi ana a Mika:
Pitoni, ndi Meleki, ndi Tareya, ndi Ahazi. 36Ndi Ahazi anabala
Yehoada, ndi Yehoada anabala Alemeti, ndi Azimaveti, ndi Zimri;
ndi Zimri anabala Moza; 37ndi Moza anabala Bineya, mwana wace
ndiye Rafa, mwana wace Eleasa, mwana wace Azeli; 38ndipo Azeli
anali nao ana asanu ndi mmodzi, maina ao ndiwo Azrikamu,
Bokeru, ndi Ismayeli, ndi Seariya, ndi Obadiya, ndi Hanani. Onsewa
ndiwo ana a Azeli. 39Ndi ana a Ezeki mbale wace: Ulamu mwana

wace woyamba, Yeusi waciwiri, ndi Elifeleti wacitatu. 40Ndipo ana a Ulamu ndiwo ngwazi zamphamvu, ndiwo oponya mibvi, nakhala nao ana ambiri ndi zidzukulu zana limodzi. Onsewa ndiwo a ana a Benjamini.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Okhala m'Yerusalemu atabwera kucokera ku Babulo

1Ndipo Aisrayeli onse anawerengedwa mwa cibadwidwe cao; ndipo
taonani, alembedwa m'buku la mafumu a Israyeli; ndipo Yuda
anatengedwa ndende kumka ku Babulo cifukwa ca kulakwa
kwao. 2Okhala m'dziko oyamba tsono, akukhala mwao mwao
m'roidzi mwao, ndiwo Israyeli, ansembe, Alevi, ndi Anetini. 3Ndipo
m'Yerusalemu munakhala a ana a Yuda, ndi a ana a Benjamini, ndi
a ana a Efraimu ndi Manase: 4Utai mwana wa Amihudi, mwana wa
Omri, mwana wa Imri, mwana wa Bani, wa ana a Perezi mwana wa
Yuda. 5Ndipo a Asiloni: Asaya woyamba, ndi ana ace. 6Ndi a ana a
Zera: Yeueli ndi abale ao mazana asanu ndi limodzi mphambu
makumi asanu ndi anai. 7Ndi a ana a Benjamini: Salu mwana wa
Mesulamu, mwana wa Hodavia, mwana wa Hasenuwa; 8ndi Ibineya
mwana wa Yerohamu, ndi Ela mwana wa Uzi, mwana-wa Mikiri, ndi
Mesulamu mwana wa Sefatiya, mwana wa Reueli, mwana wa
Ibniya, 9ndi abale ao monga mwa mibadwo yao mazana asanu ndi
anai mphambu makumi asanu kudza asanu ndi mmodzi. Onsewa
ndiwo akuru a nyumba za makolo ao m'nyumba za makolo ao.
10Ndi a ansembe: Yedaya, ndi Yehoyaribu, ndi Yakini, 11ndi Azariya
mwana wa Hilikiya, mwana wa Mesulamu, mwana wa Zadoki,
mwana wa Merayoti, mwana wa Ahitubu, mtsogoleri wa m'nyumba
ya Mulungu; 12ndi Adaya mwana wa Yerohamu, mwana wa Pasuri,
mwana wa Malikiya, ndi Maasai mwana wa Adieli, mwana wa
Yazera, mwana wa Mesulamu, mwana wa Mesilemiti, mwana wa
Imeri, 13ndi abale ao, akuru a nyumba za makolo ao cikwi cimodzi
mphambu mazana asanu ndi awiri kudza makumi asanu ndi
limodzi, anthu odziwitsitsa Debito ya utumiki wa nyumba ya
Mulungu. 14Ndi a Alevi: Semaya mwana wal Hasubu, mwana wa
Azrikamu, mwana wa Hasabiya, a ana a Merari; 15ndi Bakabakara,
Heresi, ndi Galala, ndi Mataniya mwana wa Mika, mwana wa Zikiri,
mwana wa Asafu; 16ndi Obadiya mwana wa Semaya, mwana wa
Galala, mwana wa Yedutuni, ndi Berekiya mwana wa Asa, mwana
wa Elikana, wokhala m'midzi ya Anetofati. 17Ndi odikira pakhomo:
Salumu, ndi Akubu, ndi Talimoni, ndi Ahimani ndi abate ao; Salumu
ndi mkuru wao, 18amene adadikira pa cipata ca mfumu kum'mawa
mpaka pomwepo, ndiwo odikira pakhomo a tsasa la ana a
Levi. 19Ndipo Salumu mwana wa Kore, mwana wa Ebiasafu; mwana
wa Kora, ndi abale ace a nyumba ya atate wace; Akora
anayang'anira nchito ya utumiki, osunga zipata za kacisi monga
makolo ao; anakhala m'cigono ca Yehova osunga polowera; 20ndi a
Pinehasi mwana wa Eleazara anali mtsogoleri wao kale, ndipo
Yehova anali naye. 21Zekariya mwana wa Meselemiya anali
wodikira pakhomo pa cihema cokomanako. 22Iwo onse osankhidwa

akhale odikira kuzipata ndiwo mazana awiri mphambu khumi ndi awiri. Iwo anawerengedwa monga mwa cibadwidwe cao, m'midzi mwao, amene Davide ndi Samueli mlauli anawaika m'udindo wao. 23Momwemo iwo ndi ana ao anayang'anira zipata za ku nyumba ya Yehova, ndiyo nyumba ya kacisi, m'udikiro wao. 24Pa mbali zinai panali odikira kum'mawa, kumadzulo, kumpoto, ndi kumwela. 25Ndi abale ao m'midzi mwao akafikafika, atapita masiku asanu ndi awiri masabata onse, kuti akhale nao; 26pakuti odikira anai akuru, ndiwo Alevi, anali m'udindo wao, nayang'anira zipinda ndi mosungiramo cuma m'nyumba ya Mulungu. 27Ndipo amagona usiku m'zipinda zozinga nyumba ya Mulungu, popeza udikiro wace ndi wao; kuitsegula m'mawa ndi m'mawa ndi kwaonso. 28Ndi ena a iwo anayang'anira zipangizo za utumikiwo, pakuti analowa nazo ataziwerenga, naturuka nazo ataziwerenga. 29Ndi ena a iwo anaikidwa ayang'anire zipangizo ziti zonse, ndi zipangizo zonse za malo opatulika, ndi ufa wosalala, ndi vinyo, ndi mafuta, ndi libano, ndi zonunkhira. 30Ndi ana ena a, ansembe anasanganiza cisanganizo ca zonunkhira, 31Ndi Matitiya wina wa Alevi, ndiye mwana woyamba wa Salumu Mkora, anaikidwa ayang'anire zokazingidwa m'ziwaya. 32Ndi ena a abale ao, a ana a Akohati, anayang'anira mkate woonekera, kuukonza masabata onse. 33Ndipo awa ndi oyimba akuru a nyumba za makolo a Alevi, okhala m'zipinda, omasuka ku nchito zina; pakuti anali nayo nchito yao usana ndi usiku. 34Awa ndi akuru a nyumba za makolo a Alevi mwa mibadwo yao, ndiwo akuru; anakhala ku Yerusalemu awa. 35Ndipo m'Gibeoni munakhala atate wa Gibeoni Yeieli, dzina la mkazi wace ndiye Maaka; 36ndi mwana wace woyamba ndiye Abidoni, opandana naye ndi Zuri, ndi Kisi, ndi Baala, ndi Neri, ndi Nadabu, 37ndi Gedoro, ndi Ahiya, ndi Zekariya, ndi Mikiloti. 38Ndi Mikiloti anabala Simeamu. Ndipo iwonso anakhala pamodzi ndi abale ao m'Yerusalemu, pandunji pa abale ao. 39Ndipo Neri anabala Kisi, ndi Kisi anabala Sauli, ndi Sauli anabala Yonatani, ndi Malikisuwa, ndi Abinadabu, ndi Esbaala. 40Ndipo mwana wa Yonatani ndiye Meribaala; ndi Meribaala anabala Mika. 41Ndi ana a Mika: Pitoni, ndi Meleki, ndi Tareya, ndi Ahazi. 42Ndi Ahazi anabala Yara, ndi Yara anabala Ameleti, ndi Azmaveti, ndi Zimri; ndi Zimri anabala Moza, 43ndi Moza anabala Bineya, ndi Refaya mwana wace, Eleasa mwana wace; Azeli mwana wace; 44ndi Azeli anali nao ana asanu ndi mmodzi, maina ao ndi awa; Azrikamu, Bokeru, ndi Ismayeli, ndi Seariya, ndi Obadiya, ndi Hanani; awa ndi ana a Azeli.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Za imfa ya Sauli ndi ana ace

1Afilisti tsono analimbana nkhondo ndi Israyeli; ndipo amuna a Israyeli
anathawa pamaso pa Afilisti, nagwa ophedwa pa phiri la Giliboa. 2Ndipo
Afilisti anaumirira kutsata Sauli ndi ana ace, ndi Afilistiwo anawapha Yonatani,
ndi Abinadabu, ndi Malikisuwa, ana a Sauli. 3Ndi nkhondoyi inamkulira Sauli,
ndi amauta anampeza; ndipo anatenga nkhawa cifukwa ca
amauta. 4Pamenepo Sauli anati kwa wonyamula zida zace, Solola lupanga
lako, nundipyoze nalo, angafike osadulidwa awa ndi kundiseka, Koma
wonyamula zida zace anakana, popeza anaopa kwambiri. Pomwepo Sauli
anatenga lupanga lace, naligwera. 5Ndipo pamene wonyamula zida zace
anaona kuti Sauli wafa, anagwera nayenso lupanga lace, nafa. 6Momwemo
anafa Sauli, ndi ana ace atatu; ndi nyumba yace yonse idafa pamodzi. 7Ndipo
pamene amuna onse a Israyeli okhala m'cigwamo anaona kuti anathawa, ndi
kuti Sauli ndi ana ace adafa, anasiya midzi yao, nathawa; nadza Afilisti,
nakhala m'menemo.
8Ndipo m'mawa mwace anafika Afilisti kubvula za ophedwa, napeza Sauli ndi
ana ace adagwa pa phiri la Giliboa. 9Ndipo anambvula natenga mutu wace,
ndi zida zace, natumiza ku dziko la Afilisti pozungulirapo, kulalika m'mafano
ao ndi mwa anthu. 10Ndipo anaika zida zace m'nyumba ya milungu yao,
napacika mutu wace m'nyumba ya Dagoni. 11Ndipo onse a Yabesi Gileadi,
atamva zonse Afilisti adacitira Sauli, 12anauka ngwazi zonse, nacotsa mtembo
wa Sauli, ndi mitembo ya ana ace, nabwera nayo ku Yabesi, naika mafupa ao
patsinde pa mtengo wathundu ku Yabesi, nasala masiku asanu ndi
awiri. 13Momwemo Sauli anafa, cifukwa ca kulakwa kwace analakwira Yehova,
kulakwira mau a Yehova amene sanawasunga; ndiponso cifukwa ca kufunsira
wobwebweta, kufunsirako, 14osafunsira kwa Yehova; cifukwa cace anamupha,
napambutsira ufumu kwa Davide mwana wa Jese.

Davide atalowa ufumu alanda Yerusalemu

1Pamenepo Aisrayeli onse anasonkhana kwa Davide ku Hebroni,
ndi kuti, Taonani, ife ndife pfupa lanu, ndi mnofu wanu. 2Ngakhale
kale lomwe, pokhala mfumu Sauliyo, woturuka ndi kulowa nao
Aisrayeli ndinu; ndipo Yehova Mulungu wanu anati kwa inu,
Uzidyetsa anthu anga Aisrayeli, nukhale mtsogoleri wa anthu anga
Israyeli. 3Akuru onse omwe a Israyeli anadza kwa mfumu ku
Hebroni; ndipo Davide anapangana nao pangano ku Hebroni
pamaso pa Yehova; ndipo anamdzoza Davide akhale mfumu ya
Israyeli monga mwa mau a Yehova, ndi lizanja la
Samueli. 4Namuka Davide ndi Aisrayeli onse naye ku Yerusalemu,
ndiwo Yebusi; ndipo Ayebusi nzika za m'dziko zinali
komweko. 5Ndipo nzika za m'Yebusi zinati kwa Davide, Sungalowe
muno. Koma Davide analanda linga la Ziyoni, ndiwo mudzi wa
Davide. 6Nati Davide, Ali yense woyamba kukantha Ayebusi,
yemweyo adzakhala mkulu ndi mtsogoleri. Nayamba kukwerako
Yoabu mwana wa Zeruya, nakhala mkuru iyeyu. 7Ndipo Davide
anakhala m'lingamo; cifukwa cace analicha mudzi wa
Davide. 8Ndipo anamanga mudzi pozungulira pace, kuyambira ku
Milo ndi pozungulira pace; ndi Yoabu anakonzanso potsala pa
mudzi. 9Ndipo Davide anakula-kulabe, pakuti Yehova wa makamu
anali naye.

Amphamvu a Davide

10Akuru a amphamvu aja Davide anali nao akulimbika pamodzi
naye m'ufumu wace, pamodzi ndi Aisrayeli onse, kumlonga ufumu,
monga mwa mau a Yehova akunena za Israyeli, ndi
awa. 11Kuwerenga kwa amphamvu aja Davide anali nao ndi uku:
Yasobeamu mwana wa Mhakimoni, mkuru wa makumi atatu aja,
anasamulira mazana atatu mkondo wace, nawapha nthawi
imodzi. 12Ndi pambuyo pace Eleazara mwana wa Dodo M-ahohi,
ndiye mmodzi wa atatu aja amphamvu. 13Anali pamodzi ndi Da
vide ku Pasidamimu muja; Afilisti anasonkhanako kunkhondo
kumene kunali munda wodzala ndi barele; ndipo anthu anathawa
pamaso pa Afilisti. 14Koma anadziimika pakati pa munda,
naulanditsa, nakantha Afilisti; m'mwemo anawapulumutsa Yehova
ndi cipulumutso cacikuru. 15Ndipo atatu a akuru makumi atatu
anatsikira kuthanthwe kwa Davide, ku phanga la Adulamu; ndi
nkhondo ya Afilisti idamanga misasa m'cigwa ca
Refaimu. 16Pamenepo Davide anali m'linga, ndi boma la askari
linali ku Betelehemu. 17Ndipo Davide analakalaka, nati, Ha!
mwenzi wina atandimwetsa madzi a m'citsime ca ku Betelehemu
ciri kucipata, 18Napyola atatuwo misasa ya Afilish natunga madzi
ku citsime ca ku Betelehemu ciri kucipata, nabwera nao kwa

Davide; koma Davide anakana kumwako, koma anawathirira kwa
Yehova; 19nati, Pali Mulungu wanga, kukhale kutali kwa ine kucita
ici. Ngati ndidzamwa mwazi wa anthu awa? Akadataya moyo wao,
inde akadataya moyo wao, pakukatenga madziwa. M'mwemo
sanafuna kuwamwa. Izi anazicita atatu amphamvuwa. 20Ndipo
Abisai mbale wa Yoabu, ndiye wamkuru wa atatuwa; pakuti
anasamulira mazana atatu mkondo wace, nawapha, namveka
dzina pakati pa atatuwa. 21Mwa atatuwa iye anali waulemu woposa
awiriwa, nasanduka mkuru wao; koma sanafikana nao atatu
oyamba aja. 22Benaya mwana wa Yehoyada, mwana wa ngwazi ya
ku Kabzeeli, wocita zazikuru, anapha ana awiri a Ariyeli wa ku
Moabu; anatsikanso, napha mkango m'kati mwa dzenje nyengo ya
cipale cofewa. 23Anaphanso M-aigupto munthu wamkuru, msinkhu
wace mikono isanu, ndi m'dzanja la M-aigupto munali mkondo
ngati mtanda woombera nsaru; ndipo anamtsikira ndi ndodo,
nakwatula mkondo m'dzanja la M-aigupto, namupha ndi mkondo
wace womwe. 24Izi anazicita Benaya mwana wa Yehoyada,
namveka dzina mwa atatu amphamvuwo. 25Taonani, anali wa
ulemu woposa makumi atatuwo, koma sanafikana atatu oyamba
aja; ndipo Davide anamuika mkuru wa olindirira ace.
26Ndipo amphamvuwo a magulu a nkhondo ndiwo Asaheli mbale
wa Yoabu, Elanani mwana wa Dodo wa ku Betelehemu, 27Samoti
Mharori, Helezi Mpeloni, 28Ira mwana wa Ikesi wa ku Tekoi, Abiezeri
wa ku Anatoti, 29Sibekai Mhusati, liai M-ahohi, 30Maharai Mnetofati,
Heledi mwana wa Bana Mnetofati, 31Itai mwana wa Ribai wa
Gibeya wa ana a Benjamini, Benaya Mpiratoni, 32Horai wa ku
mitsinje ya Gaasi, Abiyeli M-ariba, 33Azmaveti Mbaharumi, Eliaba
Mshaliboni; 34ana a Hasemu Mgizoni; Yonatani mwana wa Sage
Mharari, 35Ahiamu mwana wa Sakari Mharari, Elifali mwana wa
Uri, 36Heferi Mmekerati, Ahiya Mpeloni, 37Hezro wa ku Karimeli,
Naarai mwana wa Ezbai, 38Yoeli mbale wa Natani, Mibari mwana
wa Hagiri, 39Zeleki M-amoni, Naharai Mberoti wonyamula zida za
Yoabu mwana wa Zeruya, 40Ira M-itiri, Garebi M-itiri, 41Uriya Mhiti,
Zabadi mwana wa Alai, 42Adina mwana wa Siza Mrubeni mkuru wa
Arubeni, ndi makumi atatu pamodzi naye, 43Hanani mwana wa
Maaka, ndi Yosafati Mmitini, 44Uziya M-asterati, Sama ndi Yeieli ana
a Hotamu wa ku Aroeri, 45Yedyaeli mwana wa Simri, ndi Yoha
mbale wace Mtizi, 46Elieli Mmahavi, ndi Yeribai ndi Yosaviya ana a
Elinaamu, ndi Itima Mmoabu, 47Elieli, ndi Obedi, ndi Yasiyeli
Mmezobai.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Amphamvu anadza kwa Davide namtsata pomlonda Sauli

1Anadzawo kwa Davide ku Zikilaga, akali citsekedwere cifukwa ca
Sauli mwana wa Kisi, ndi awa; ndiwo mwa amphamvuwo
omthandiza kunkhondo. 2Anakoka mauta; naponya miyala,
naponya mibvi ndi uta ndi dzanja lamanja ndi lamanzere lomwe;
ndiwo a abale ace a Sauli, Abenjamini. 3Mkuru wao ndiye Ahiezeri,
ndi Yoasi, ana a Semaa wa ku Gibeya; ndi Yezieli, ndi Peleti, ana a
Azmaveti; ndi Beraka, ndi Yehu wa ku Anatoti, 4ndi Ismaya wa ku
Gibeoni, wamphamvu mwa makumi atatuwo ndi woyang'anira
makumi atatuwo, ndi Yeremiya, ndi Yahazieli, ndi Yohanani, ndi
Yozabadi wa ku Gedera, 5Eluzai, ndi Yerimoti, ndi Bealiya, ndi
Semariya, ndi Sefatiya wa ku Harupi, 6Elikana, ndi Isiya, ndi
Azereli, ndi Yoezeri, ndi Yasobeamu ndiwo Akora; 7ndi Yoda, ndi
Zebadiya, ana a Yerohamu wa ku Gedoro. 8Ndi Agadi ena
anapambukira kwa Davide ku liogala m'cipululu, ngwazi
zamphamvu zozerewera nkhondo, zogwira cikopa ndi mkondo;
nkhope zao zikunga nkhope za mikango, ndi liwiro lao longa la
ngoma kumapiri: 9Ezeri mkuru wao, waciwiri Obadiya, wacitatu
Eliabu, 10wacinai Misimana, wacisanu Yeremiya, 11wacisanu ndi
cimodzi Atai, wacisanu ndi ciwiri Elieli, 12wacisanu ndi citatu
Yohanani, wacisanu ndi cinai Elzabadi, 13wakhumi Yeremiya,
wakhumi ndi cimodzi Makibanai. 14Awa a ana a Gadi, anali
atsogoleri a nkhondo; wamng'ono wa iwo anayang'anira zana
limodzi, ndi wamkuru wa iwo anayang'anira cikwi cimodzi. 15Awa
ndi omwe aja anaoloka Yordano mwezi woyamba, atadzala
kusefukira magombe ace onse; nathawitsa onse okhala m'zigwa
kum'mawa ndi kumadzulo. 16Ndipo anadza ena a ana a Benjamini
ndi Yuda kulinga kwa Davide. 17Ndipo Davide anaturuka kukomana
nao, nayankha, nanena nao, Ngati mwandidzera mwamtendere
kundithandiza, mtima wanga udzalumikizana nanu; koma ngati
mwafika kundipereka kwa adani anga, popeza m'manja mwanga
mulibe ciwawa, Mulungu wa makolo athu acione ndi
kucilanga. 18Pamenepo mzimu unabvala Amasai, ndiye wamkuru
wa makumi atatuwo, nati iye, Ndife anu, Davide, tibvomerezana
nanu mwana wa Jese inu: mtendere, mtendere ukhale ndi inu, ndi
mtendere ukhale ndi athandizi anu; pakuti Mulungu wanu
akuthandizani. Ndipo Davide anawalandira, nawaika akuru a
magulu. 19Ena a Manase omwe anapambukira kwa Davide, muja
iye anadza ndi Afilisti koponyana nkhondo ndi Sauli, koma
sanawathandiza; popeza akalonga a Afilisti, atacita upo, anamuuza
acoke, ndi kuti, Adzapambukira kwa mbuye wace Sauli ndi
kutisandulikira. 20Pomuka iye ku Zikilaga anapambukira kwa iye a
Manase: Adina, ndi Yozabadi, ndi Yedyaeli, ndi Mikaeli, ndi

Yozabadi, ndi Elihu, ndi Ziletai, akuru a zikwi a ku Manase. 21Ndipo
anathandiza Davide aponyane nalo gulu la acifwamba, pakuti onse
ndiwo ngwazi zamphamvu, nakhala atsogoleri m'khamu la
nkhondo. 22Pakuti nthawi yomweyo anadza kwa Davide
kumthandiza, mpaka kunali nkhondo yaikuru; ngati nkhondo ya
Mulungu.

Akuru omponya Davide mfumu: ku Hebroni

23Ndipo kuwerenga kwa akuru okonzekeratu kunkhondo, anadzawo
kwa Davide ku Hebroni, kupambukitsa ufumu wa Sauli ukhale
wace, monga mwa mau a Yehova, ndi: uku. 24Ana a Yuda
akunyamula zikopa ndi mikondo ndiwo zikwi zisanu ndi cimodzi
mphambu mazana asanu ndi atatu, okonzekeratu kunkhondo. 25A
ana a Simeoni ngwazi zamphamvu za nkhondo zikwi zisanu ndi
ziwiri mphambu zana liimodzi. 26A ana a Levi zikwi zinai mphambu
mazana asanu ndi limodzi. 27Ndipo Yehoyada, ndiye mtsogoleri wa
Aaroni, ndi pamodzi nave zikwi zitatu mphambu mazana asanu ndi
awiri; 28ndi Zadoki, ndiye mnyamata, ngwazi yamphamvu, ndi a
nyumba ya kholo lace, akuru makumi awiri mphambu awfri. 29Ndi
a ana a Benjamini, abale a Sauli, zikwi zitatu; pakuti mpaka
pomwepo ocuruka a iwowa anaumirira nyumba ya Sauli. 30Ndi a
ana a Efraimu zikwi makumi awiri mphambu mazana asanu ndi
atatu, ngwazi zamphamvu, anthu omveka m'nyumba za makolo
ao. 31Ndipo a pfuko la Manase logawika pakati zikwi khumi
mphambu zisanu ndi zitatu, ochulidwa maina ao kuti adzalonge
Davide mfumu. 32Ndi a ana a Isakara, anthu akuzindikira nyengo,
akudziwa zoyenera Israyeli kuzicita, akuru ao ndiwo mazana awiri;
ndi abale ao onse anapenyerera pakamwa pao. 33A Zebuloni
akuturuka kukhamu, opangira nkhondo, monga mwa zida ziri
zonse za nkhondo, zikwi makumi asanu, akusunga
malongosoledwe a nkhondo ndi mtima wosatekeseka. 34Ndi a
Nafitali atsogoleri cikwi cimodzi, ndi pamodzi nao ogwira zikopa ndi
mikondo zikwi makumi atatu mphambu zisanu ndi ziwiri. 35Ndi a
Adani akupangira nkhondo zikwi makumi awiri mphambu zisanu
ndi zitatu kudza mazana asanu ndi limodzi. 36Ndi a Aseri akuturuka
kukhamu, akupangira nkhondo, zikwi makumi anai. 37Ndi tsidya lga
la Yordano a Arubeni, ndi Agadi, ndi pfuko la: Manase logawika
pakati, ndi zida: ziri zonse za khamu kucita nazo nkhondo, zikwi
zana limodzi ndi makumi awiri. 38Onsewa, ndiwo anthu a nkhondo
akusunga malongosoledwe a nkhondo, anadza ku Hebroni ndi
mtima wangwiro kudzamlonga Davide mfumu ya Aisraeli onse; ndi
onse otsala a Israyeli omwe anali a mtima umodzi kumlonga
Davide ufumu. 39Ndipo anali komweko kwa Davide masiku atatu
kudya ndi kumwa, popeza abale ao-anazikonzeratu. 40Ndiponso
akuyandikizana nao mpaka Isakara ndi Zebuloni ndi Nafitali

anabwera nao mkate osenzetsa aburu, ndi ngamira, ndi nyuru, ndi ng'ombe, zakudya zaufa, ndi ncinci zankhuyu, ndi ncinci zamphesa, ndi vinyo, ndi mafuta, ndi ng'ombe, ndi nkhosa zocuruka; pakuti munali cimwemwe m'Israyeli.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Apita nalo likasa nalisunga m'nyumba ya Obedi Edomu

1Ndipo Davide anafunsana ndi akuru a zikwi ndi a mazana, inde
atsogoleri ali onse. 2Ndipo Davide anati kwa msonkhano wonse wa
Israyeli, Cikakomera inu, ndipo cikacokera kwa Yehova Mulungu
wathu, titumize konse kuti abale athu otsala m'dziko lonse la
Israyeli, ndi ansembe ndi Alevi okhala nao m'midzi yao yokhala
napa podyetsa, kuti asonkhane kwa ife; 3ndipo tibwere nalo kwa
ife likasa la Mulungu wathu, pakuti sitinafunako masiku a
Sauli. 4Ndipo a msonkhano onse anati kuti adzacita; pakuti
cidayenera cinthuci pamaso pa anthu onse. 5M'mwemo Davide
anamemeza Aisrayeli onse kuyambira Sihori wa ku Aigupto mpaka
polowera ku Hamati, kutenga likasa la Mulungu ku Kiriati-
Yearimu. 6Ndipo Davide ndi Aisrayeli onse pamodzi naye anakwera
kumka ku Baala, ndiko ku Kiriati-Yearimu wa m'Yuda, kukwera nalo
kucokera komweko likasa la Mulungu Yehova wakukhala pa
akerubi, kumene aitanirako Dzina. 7Ndipo anatengera likasa la
Mulungu pa gareta watsopano kucokera ku nyumba ya Abinadabu;
ndi Uza ndi Ahiyo anayendetsa ng'ombe za pa garetayo, 8Ndipo
Davide ndi Aisrayeli onse anasewera pamaso pa Mulungu ndi
mphamvu yao yonse; ndi nyimbo, ndi azeze, ndi zisakasa, ndi
malingaka, ndi nsanje, ndi malipenga, 9Ndipo pamene anafika ku
dwale la Kidoni, Uza anatambasula dzanja lace kulicirikiza likasa,
pakuti ng'ombe zikadapulumuka. 10Ndi mkwiyo wa Yehova
unayakira Uza, namkantha, cifukwa anatambasulira likasa dzanja
lace, nafa komweko pamaso pa Mulungu. 11Ndipo kudaipira Davide
kuti Yehova adacita cipasulo ndi Uza; motero anacha malowo
Perezi Uza, mpaka lero lino. 12Ndipo Davide anaopa Mulungu
tsikulo, ndi kuti, Ndidzafika nalo bwanji likasa la Mulungu
kwathu? 13M'mwemo Davide sanafika nalo likasa kwao ku mudzi
wa Davide, koma analipambutsira ku nyumba ya Obedi Edomu wa
ku Giti. 14Ndi likasa la Mulungu linakhala ndi banja la Obedi Edomu
m'nyumba mwace miyezi itatu; ndipo Yehova anadalitsa nyumba
ya Obedi Edomu, ndi zonse anali nazo.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Cibwenzi ca Hiramu, kulephera kwa Afilisti

1Ndipo Hiramu mfumu ya Turo anatumiza mithenga kwa Davide,
ndi mikungudza, ndi amisiri omanga miyala, ndi amatabwa, kuti
ammangire nyumba. 2Ndipo Davide anazindikira kuti Yehova
adamkhazikitsa mfumu ya Israyeli; pakuti ufumu wace
unakwezekadi, cifukwa ca anthu ace Israyeli.
3Ndipo Davide anatenga akazi ena ku Yerusalemu, nabala Davide
ana amuna ndi akazi ena. 4Maina a ana anali nao m'Yerusalemu
ndi awa: Samna, ndi Sobabu Natani, ndi Solomo, 5ndi Ibara, ndi
Elisua, ndi Elipeleti, 6ndi Noga, ndi Nefegi, ndi Yafiya, 7ndi Elisama,
ndi Beliyada, ndi Elifeleti.
8Pamene Afilisti anamva kuti anamdzoza Davide akhale mfumu ya
Aisrayeli onse, Afilisti onse anakwera kufunafuna Davide; ndipo
Davide anamva, nawaturukira. 9Afilisti tsono anafika, nafalikira
m'cigwa ca Refaimu. 10Ndipo Davide anafunsira kwa Mulungu, kun,
Ndikwere kodi kuyambana ndi Afilisti? mudzawapereka m'dzanja
langa kodi? Ndipo Yehova anati kwa iye, Kwera, pakuti
ndidzawapereka m'dzanja lako. 11Atafika tsono ku Baala Perazimu,
Davide anawakantha komweko; nati Davide, Mulungu anapasula
adani anga ndi dzanja langa, ngati pokhamulira madzi. Cifukwa
cace analicha dzina la malowo Baala Perazimu. 12Ndipo anasiyako
milungu yao; nalamula Davide, ndipo anaitentha ndi moto. 13Ndipo
Afilisti anabwerezanso, nafalikira m'cigwamo. 14Ndipo Davide
anafunsiranso kwa Mulungu, nanena Mulungu naye, Usakwera
kuwatsata, uwazungulire, nuwadzere pandunji pa mitengo ya
mkandankhuku. 15Ndipo kudzali, pakumva iwe kuwayula kunsonga
kwa mitengo ya mkandankhuku, pamenepo uturukire kunkhondo;
pakuti Mulungu waturukira pamaso pako kukantha gulu la
Afilisti. 16Nacita Davide monga Yehova adamuuza, nakantha gulu
la Afilisti kuyambira ku Gibeoni kufikira ku Gezeri. 17Ndipo mbiri ya
Davide inabuka m'maiko onse, nafikitsira Yehova kuopsa kwace pa
amitundu onse.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Davide afikitsa, likasa ku Yerusalemu, nalongosola mapembedzedwe

1Ndipo Davide anadzimangira nyumba m'mudzi mwace,
nakonzeratu malo likasa la Mulungu, naliutsira hema. 2Pamenepo
Davide anati, Sayenera ena kusenza likasa la Mulungu koma Alevi
ndiwo; pakuti Yehova anawasankha iwo kusenza likasa la Mulungu,
ndi kumtumikira iye kosatha. 3Ndipo Davide anasonkhanitsira
Aisrayeli onse ku Yerusalemu, akwere nalo likasa la Yehova kumalo
kwace adalikonzera. 4Ndipo Davide anasonkhanitsa ana a Aroni ndi
Alevi; 5a ana a Kohati, Urieli mkuru wao, ndi abale ace zana limodzi
mphambu makumi awiri; 6a ana a Merari, Adaya mkuru wao, ndi
abale ace mazana awiri mphambu makumi awiri; 7a ana a
Gerisomu, Yoeli mkuru wao, ndi abale ace zana limodzi mphambu
makumi atatu; 8a ana a Elizafana, Semaya mkuru wao, ndi abale
ace mazana awiri; 9a ana a Hebroni, Elieli mkuru wao, ndi abale
ace makumi asanu ndi atatu; 10a ana a Uzieli, Aminadabu mkuru
wao, ndi abale ace zana limodzi mphambu khumi ndi
awiri. 11Ndipo anaitana Zadoki ndi Abyatara ansembe, ndi Alevi
Urieli, Asaya, ndi Yoeli, Semaya, ndi Elieli, ndi Aminadabu, nanena
nao, 12Inu ndinu akuru a nyumba za makolo a Alevi, mudzipatule
inu ndi abale anu omwe, kuti mukatenge ndi kukwera nalo likasa la
Yehova Mulungu wa Israyeli ku malo ndalikonzera. 13Pakuti,
cifukwa ca kusalinyamula inu poyamba paja, Yehova Mulungu
wathu anacita cotipasula, popeza sitinamfunafuma Iye monga
mwa ciweruzo. 14Momwemo ansembe ndi Alevi anadzipatula kuti
akwere nalo likasa la Yehova Mulungu wa Israyeli. 15Ndipo ana a
Alevi anasenza likasa la Mulungu pa mapewa ao, mphiko ziri
m'mwemo, monga Mose anawauza, monga mwa mau a
Yehova. 16Ndipo Davide ananena ndi mkuru wa Alevi kuti aike
abale ao oyimbawo ndi zoyimbira, zisakasa, ndi azeze, ndi nsanje,
azimveketse ndi kukweza mau ao ndi cimwemwe. 17Ndipo Alevi
anaika Hemani mwana wa Yoeli, ndi a abale ace Asafu mwana wa
Berekiya, ndi a ana a Merari, abale ao, Etani mwana wa
Kusaya; 18ndi pamodzi nao abale ao a kulongosola kwaciwiri,
Zekariya, Beni, ndi Yaazieli, ndi Semiramoti, ndi Yehieli, ndi Uni,
Bliabu, ndi Benaya, ndi Maaseya, ndi Matitiya, ndi Blifelehu, ndi
Mikineya, ndi Obedi Bdomu, ndi Yeieli, ndikirawo. 19Oyimba tsono:
Hemani, Asafu, ndi Btani, anayimba ndi nsanje zamkuwa; 20ndi
Zekariya, ndi Azieli, ndi Semiramod, ndi Yehieli, ndi Uni, ndi Bliabu,
ndi Maaseya, ndi Benaya, ndi zisakasa kuyimbira mwa
Alimoti; 21ndi Matitiya, ndi Elifelehu, ndi Mikeya, ndi Obedi Edomu,
ndi Yeieli, ndi Azaziya, ndi azeze akuyimbira mwa Seminiti,
kutsogolera mayimbidwe. 22Ndi Kenaniya mkuru wa Alevi

anayang'anira kusenzako; anawalangiza za kusenza, pakuti anali waluso. 23Ndi Berekiya ndi Elikana anali odikira likasa. 24Ndi Sebaniya, ndi Yosafati, ndi Netaneli, ndi Amasai, ndi Zekariya, ndi Benaya, ndi Eliezere, ansembe, analiza malipenga ku likasa la Mulungu; ndi Obedi Edomu ndi Yehiya anali odikira a likasa. 25Momwemo Davide, ndi akuru akuru a Israyeli, ndi atsogoleri a zikwi, anamuka kukwera nalo likasa la cipangano la Yehova, kucokera ku nyumba ya Obedi Edomu mokondwera. 26Ndipo popeza Mulungu anathandiza Alevi akusenza likasa la cipangano la Yehova, iwo anapha nsembe ng'ombe zisanu ndi ziwiri, ndi nkhosa zamphongo zisanu ndi ziwiri. 27Ndipo Davide anabvala maraya abafuta, ndi Alevi onse akunyamula likasa, ndi oyimba, ndi Kenaniya woyang'anira kusenzaku, pamodzi ndi oyimba; Davide anabvalanso efodi wabafuta. 28Momwemo Aisrayeli onse anakwera nalo likasa la cipangano la Yehova ndi kupfuula, ndi kumveka kwa lipenga, ndi mphalasa, ndi nsanje zomveketsa, ndi zisakasa, ndi azeze. 29Ndipo polowa likasa la cipangano la Yehova m'mudzi wa Davide, Mikala mwana wamkazi wa Sauli anasuzumira pazenera, naona mfumu Davide alikutumphatumpha ndi kusewera; ndipo anampeputsa mumtima mwace.

©The Bible Society of Malawi, 1992

1Ndipo analowa nalo likasa la Mulungu, nalgka pakati pa hemalo
Davide adaliutsira; ndipo anapereka nsembe zopsereza ndi nsembe
zoyamika pamaso pa Mulungu. 2Ndipo atatha Davide kupereka
nsembe zopsereza ndi nsembe zoyamika, anadalitsa anthu m'dzina
la Yehova. 3Nagwira ali yense wa Israyeli, wamwamuna ndi
wamkazi, yense mtanda wa mkate, ndi nthuli ya nyama, ndi ncinci
ya mphesa zouma.
4Ndipo anaika Alevi ena atumikire ku likasa la Yehova, nalalikire,
nayamike, nalemekeze Yehova Mulungu wa Israyeli. 5Asafu ndiye
mkuru wao, ndi otsatana naye Zekariya, Yeieli, ndi Semiramoti, ndi
Yehieli, ndi Matitiya, ndi Eliabu, ndi Benaya, ndi Obedi Edomu, ndi
Yeieli, ndi zisakasa ndi azeze; koma Asafu ndi nsanje
zomvekatu; 6ndi Benaya ndi Yahazieli ansembe ndi malipenga
kosalekeza, ku likasa la cipangano la Mulungu.

Salmo la Davide

7Tsiku limenelo tsono Davide anayamba kuwapatsa nyimbo ya
kuyamika nayo Yehova; ocita ndiwo Asafu ndi abale ace.
8Yamikani Yehova, itanani dzina lace;
Bukitsani mwa mitundu ya anthu zocita iye.
9Myimbireni, myimbireni zomlemekeza;
Fotokozerani zodabwiza zace zonse.
10Mudzitamandire ndi dzina lace lopatulika;
Mitima yao ya iwo ofuna Yehova ikondwere.
11Funsirani kwa Yehova ndi mphamvu yace;
Funani nkhope yace nthawi zonse.
12Kumbukilani zodabwiza zace adazicita,
Zizindikilo zace, ndi maweruzo a pakamwa pace;
13Inu mbeu ya Israyeli mtumiki wace,
Inu ana a Yakobo, osankhika ace.
14Iye ndiye Yehova Mulungu wathu;
Maweruzo ace akhala pa dziko lonse lapansi,
15Kumbukilani cipangano cace kosatha,
Mauwo anawalamulira mibadwo zikwi;
16Cipanganoco anapangana ndi Abrahamu,
Ndi lumbiro lace ndi Isake;
17Ndipo anacitsimikizirakwa Yakobo cikhale malemba,
Cikhale cipangano cosatha kwa Israyeli;
18Ndi kunena kuti, Ndidzakupatsa iwe dziko la Kanani,
Gawo la colandira cako;
19Pokhala inu anthu owerengeka,
Inde anthu pang'ono, ndi alendo m'mwemo;
20Nayendayenda kucokera mtundu wina kufikira mtundu wina,
Kucokera ufumu wina kufikira anthu ena.

21Sanalola munthu awasautse;
Ndipo anadzudzula mafumu cifukwa ca iwowa;
22Ndi kuti, Musamakhudza odzozedwa anga,
Musamacitira coipa aneneri anga,
23Myimbireni Yehova, inu dziko lonse lapansi,
Lalikirani cipulumutso cace tsiku ndi tsiku,
24Fotokozerani ulemerero wace mwa amitundu,
Zodabwiza zace mwa mitundu yonse ya anthu.
25Pakuti Yehova ali wamkuru, nayenera kulemekezedwa kwakukulu;
Ayenera amuope koposa milungu yonse.
26Pakuti milungu ya mitundu ya anthu ndiyo mafano;
Koma Yehova analenga zakumwamba.
27Pamaso pace pali ulemu ndi ukulu,
M'malo mwace muli mphamvu ndi cimwemwe.
28Mcitireni Yehova, inu mafuko a mitundu ya anthu,
Mcitireni Yehova ulemerero ndi mphamvu.
29Mcitireni Yehova ulemerero wa dzina lace;
Bwerani naco copereka, ndipo fikani pamaso pace;
Lambirani Yehova m'ciyero cokometsetsa,
30Njenjemerani pamaso pace, inu dziko lonse lapansi,
Dziko lokhalamo anthu lomwe lakhazikika, kuti silingagwedezeke.
31Kukondwerere kumwamba, ndi dziko lapansi lisekerere;
Anene mwa amitundu, Yehova acita ufumu.
32Nyanja ikukume m'kudzala kwace,
Munda ukondwerere, ndi zonse ziri m'mwemo;
33Pamenepo mitengo yonse ya kunkhalango idzapfuula
mokondwera pamaso pa Yehova;
Pakuti akudza kudzaweruza dziko lapansi,
34Yamikani Yehova; pakuti iye ndiye wabwino;
Pakuti cifundo cace ncosatha.
35Nimunene, Tipulumutseni, Mulungu wa cipulumutso cathu;
Mutisokolotse ndi kutilanditsa kwa amitundu,
Kuti tiyamike dzina lanu loyera,
Ndi kudzitamandira naco cilemekezo canu.
36Alemekezedwe Yehova Mulungu wa Israyeli,
Kuyambira kosayamba kufikira kosatha.
Ndipo anthu onse anati, Amen! nalemekeza Yehova.

Cihema cosonkhanako cikhala ku Gibeoni

37Ndipo anasiyako ku likasa la cipangano la Yehova Asafu ndi abale ace, atumikire kulikasa kosalekeza, monga umo mudzafunika tsiku ndi tsiku; 38ndi Obedi Edomu, ndi abale ace makumi asanu ndi limodzi mphambu asanu ndi atatu; ndi Obedi Edomu mwana wa Yedutuni ndi Hosa akhale odikira; 39ndi Zadoki wansembe, ndi abale ace ansembe, ku kacisi wa Yehova, pa msanje unali ku

Gibeoni; 40kupereka nsembe zopsereza kwa Yehova pa guwa la
nsembe zopsereza, kosalekeza, m'mawa ndi madzulo, monga mwa
zonse zilembedwa m'cilamulo ca Yehova adacilamulira
Israyeli; 41ndi pamodzi nao Hemani, ndi Yedutuni, ndi osankhika
otsalawo, ochulidwa maina, kuyamika Yehova; pakuti cifundo cace
ncosatha; 42ndi pamodzi nao Hemani, ndi Yedutuni, ndi malipenga
ndi nsanje za iwo akumveketsadi, ndi zoyimbira nyimbo za
Mulungu; ndi ana a Yedutuni anakhala kucipata. 43Ndipo anacoka
anthu onse, yense ku nyumba yace, nabwera Davide kudalitsa
nyumba yace.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Yehova salola Davide ammangire Kacisi

1Ndipo pokhala Davide m'nyumba mwace, Davideyo anati kwa
Natani mneneri, Taona, ndikhala ine m'nyumba yamikungudza,
koma Gkasa la cipangano likhala m'nsaru zocinga. 2Ndipo Natani
anati kwa Davide, Mucite zonse ziri m'mtima mwanu; pakuti
Mulungu ali nanu. 3Ndipo usiku womwewo mau a Mulungu
anadzera Natani, ndi kuti, 4Kauze Davide mtumiki wanga, Atero
Yehova, Usandimangire nyumba yokhalamo; 5pakuti sindinakhala
m'nyumba kuyambira tsiku tija ndinakwera naye Israyeli, kufikira
lero Gno; koma wa m'hema m'hema Ine, ndi wa m'kacisi
m'kacisi, 6Pali ponse ndinayenda nao Aisrayeli onse ndinanena kodi
mau ndi woweruza ali yense wa Israyeli, amene ndinamuuza
adyetse anthu anga, ndi kuti, Mwalekeranji kundimangira nyumba
yamikungudza? 7Cifukwa cace tsono, uzitero naye mtumiki wanga
Davide, Atero Ambuye wa makamu, Ndinakutenga kubusa potsata
iwe nkhosa, kuti ukhale mtsogoleri wa anthu anga Israyeli; 8ndipo
ndakhala ndi iwe kuli konse unamukako, ndi kuononga adani ako
onse pamaso pako; ndipo ndakubukitsira dzina lakunga dzina la
akuru okhala padziko. 9Ndipo ndaikira anthu anga Israyeli malo,
ndi kuwaoka, kuti akhale m'malo mwao osasunthikanso; ndi ana
osalungama sadzawapululanso monga poyamba paja; 10ndi
kuyambira kuja ndinaika oweruza ayang'anire anthu anga Israyeli;
ndipo ndagonjetsa adani ako onse. Ndikuuzanso kuti Yehova
adzakumangira banja. 11Ndipo kudzacitika, atakwanira masiku ako
kuti uzipita kukhala ndi makolo ako, ndidzaukitsa mbeu yako
pambuyo pako, ndiye wa ana ako; ndipo ndidzakhazikitsa ufumu
wace. 12Iye adzandimangira nyumba; ndipo ndidzakhazikitsa
mpando wacifumu wace kosatha. 13Ndidzakhala atate wace, ndi
iye adzakhala mwana wanga; ndipo sindidzamcotsera cifundo
canga monga muja ndinacotsera iye amene anakhala usanakhale
iwe; 14koma ndidzamkhazikitsa m'nyumba mwanga, ndi m'ufumu
wanga kosatha; ndi mpando wa cifumu wace udzakhazikika
kosatha. 15Monga mwa mau awa onse, ndi monga mwa
masomphenya awa onse, momwemo Natani analankhula ndi
Davide.

Conena Davide

16Pamenepo mfumu Davide analowa nakhala pamaso pa Yehova,
nati, Ndine yani, Yehova Mulungu, ndi nyumba yanga njotani kuti
mwandifikitsa mpaka pano? 17Ndipo ici ncacing'ono pamaso panu,
Mulungu, koma mwanena za nyumba ya mtumiki wanu nthawi
yam'tsogolo ndithu, ndipo mwandiyesera ngati munthu womveka,
Yehova Mulungu. 18Anenenjinso Davide kwa Inu za ulemu
wocitikira mtumiki wanu? pakuti mudziwa mtumiki

wanu. 19Yehova, cifukwa ca mtumiki wanu, ndi monga mwa mtima
wanu, mwacita ukulu uwu wonse, kundidziwitsa zazikuru izi
zonse. 20Yehova, palibe wina wonga inu, palibenso Mulungu wina
koma Inu; monga mwa zonse tazimva m'makutu mwathu. 21Ndiwo
ayani akunga anthu anu Israyeli, mtundu wa pa wokha wa pa dziko
lapansi, amene Mulungu anakadziombolera mtundu wa anthu,
kudzibukitsira dzina, mwa zazikuru ndi zoopsa, pakupitikitsa
amitundu pamaso pa anthu anu amene munawaombola
m'Aigupto? 22Pakuti anthu anu Israyeli mudawayesa anthu anu anu
kosatha; ndipo Inu, Yehova, munayamba kukhala Mulungu
wao. 23Ndipo tsopano, Yehova, akhazikike kosalekeza mau
mudanenawa za mtumiki wanu, ndi za nyumba yace, nimucite
monga mwanena. 24Inde likhazikike dzina lanu, likulitsidwe
kosalekeza, ndi kuti, Yehova wa makamu ndiye Mulungu wa
Israyeli; akhalira Israyeli Mulungu; ndi nyumba ya Davide mtumiki
wanu ikhazikika pamaso panu. 25Pakuti Inu, Mulungu wanga,
mwaululira mtumiki wanu kuti mudzammangira banja; momwemo
mtumiki wanu waona mtima wakupemphera pamaso
panu. 26Ndipo tsopano, Yehova, Inu ndinu Mulungu, ndipo
mwanenera mtumiki wanu cokoma ici; 27cakukomerani kudalitsa
nyumba ya mtumiki wanu, kuti ikhalebe kosatha pamaso panu;
pakuti Inu Yehova mwadalitsa, ndipo idzadalitsika kosatha.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Davide akantha Afilisti, Amoabu, Aaramu, ndi Aedomu

1Ndipo zitatha izi, Davide anakantha Afilisti, nawagonjetsa,
nalanda Gati ndi midzi yace m'manja a Afilisti. 2Anakanthanso
Moabu; ndi Amoabu anakhala anthu a Davide, nabwera nazo
mphatso, 3Ndipo Davide anakantha Hadarezeri mfumu ya Zoba ku
Hamati, pomuka iye kukhazikitsa ulamuliro wace ku mtsinje wa
Firate. 4Ndipo Davide analanda magareta ace cikwi cimodzi, ndi
apakavalo zikwi zisanu ndi ziwiri, ndi oyenda pansi zikwi makumi
awiri; Davide anadula mitsita akavalo onse okoka magareta, koma
anasungako ofikira magareta zana limodzi. 5Ndipo Aaramu a ku
Damasiko anadza kudzathandiza Hadarezeri mfumu ya Zoba;
koma Davide anakantha Aaramu amuna zikwi makumi awiri
mphambu ziwiri. 6Ndipo Davide anaika asilikari a boma m'Aramu
wa Damasiko; ndi Aaramu anasanduka anthu a Davide, nabwera
nazo mphatso, Ndipo Yehova anasunga Davide kuli konse
anamukako. 7Natenga Davide zikopa zagolidi zinali pa anyamata a
Hadarezeri, nabwera nazo ku Yerusalemu. 8Ndi ku Tibati, ndi ku
Kuni, midzi ya Hadarezeri, Davide anatenga mkuwa wambiri, ndiwo
umene Solomo anayenga nao thawale lamkuwa, ndi nsanamira,
ndi zipangizo zamkuwa. 9Ndipo pakumva Tou, mfumu ya ku
Hamati, kuti Davide adakantha khamu lonse la Hadarezeri mfumu
ya ku Zoba, 10anatumiza Hadoramu mwana wace kwa Davide,
kumlankhula ndi kumdalitsa, popeza adayambana ndi Hadarezeri,
namkantha; pakuti Hadarezeri adacita nkhondo ndi Tou; ndipo
anali nazo zipangizo za mitundu mitundu za golidi ndi siliva ndi
mkuwa. 11Izi zomwe mfumu Davide anazipatulira Yehova, pamodzi
ndi siliva ndi golidi adazitenga kwa amitundu onse, kwa Edomu,
ndi kwa Moabu, ndi kwa ana a Amoni, ndi kwa Afilisti, ndi kwa
Amaleki. 12Ndipo Abisai mwana wa Zeruya anakantha Aedomu
m'Cigwa ca Mcere zikwi khumi mphambu zisanu ndi zitatu. 13Ndipo
anaika asilikari a boma m'Edomu; ndi Aedomu onse anasanduka
anthu a Davide. Ndipo Yehova anasunga Davide kuli konse
anamukako.
14Ndipo Davide anakhala mfumu ya Aisrayeli onse, naweruza
anthu ace onse, nawacitira cilungamo. 15Ndipo Yoabu mwana wa
Zeruya anayang'anira khamu la nkhondo, ndi Yehosafati mwana
wa Ahiludi anali wolemba mbiri. 16Ndi Zadoki mwana wa Ahitubu,
ndi Abimeleki mwana wa Abyatara, anali ansembe, ndi Savisa anali
mlembi, 17ndi Benaya mwana wa Yehoyada anayang'anira Akereti
ndi Apeleti; koma ana a Davide ndiwo oyamba ku dzanja la mfumu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Davide abwezera cilango kwa Aamoni pa cipongwe cao

1Ndipo zitatha izi, Nahasi mfumu ya ana a Amoni anamwalira, ndi
mwana wace anakhala mfumu m'malo mwace. 2Ndipo Davide
anati, Ndidzamcitira zokoma mtima Hanuni mwana wa Nahasi,
popeza atate wace anandicitira ine zokoma mtima. Momwemo
Davide anatuma mithenga imtonthoze mtima pa atate wace.
Pofika anyamata ace a Davide ku dziko la ana a Amoni kwa Hanuni
kumtonthoza mtima, 3akalonga a ana a Amoni anati kwa Hanuni,
Davide ali kucitira atate wanu ulemu kodi, popeza anakutumizirani
otonthoza? sakudzerani kodi anyamata ace kufunafuna, ndi
kugubuduza, ndi kuzonda dziko? 4Ndipo Hanuni anatenga
anyamata a Davide, nawameta, nadula malaya ao pakati kufikira
m'matako, nawaleka acoke. 5Pamenepo anamuka ena, namuuza
Davide za amunawa. Natumiza iye kukomana nao, pakuti
amunawa anacita manyazi kwambiri. Ndipo mfumu inati, Balindani
ku Yeriko mpaka zamera ndebvu zanu; zitamera mubwere. 6Ndipo
pamene ana a Amoni anaona kuti anadzinunkhitsa kwa Davide,
Hanuni ndi ana a Amoni anatumiza matalente cikwi cimodzi a
siliva, kudzilembera magareta ndi apakavalo ku Mesopotamiya, ndi
ku Aramu-maaka, ndi ku Zoba. 7Momwemo anadzilembera
magareta zikwi makumi atatu mphambu ziwiri, ndi mfumu ya
Maaka ndi anthu ace; nadza iwo, namanga misasa cakuno ca
Medeba. Ana a Amoni omwe anasonkhana m'midzi mwao, nadza
kunkhondo. 8Pamene Davide anamva ici anatuma Yoabu ndi gulu
lonse la anthu amphamvu. 9Ndipo ana a Amoni anaturuka,
nandandalitsa nkhondo ku cipata ca mudzi, ndi mafumu adadzawo
anali pa okha kuthengo. 10Pakuona Yoabu tsono kuti nkhondo
inamdzera kumaso ndi kumbuyo, anasankha amuna osankhika
onse a Israyeli, nawanika ayambane ndi Aaramu. 11Ndipo anthu
otsala anawapereka m'dzanja la Abisai mbale wace; ndipo
anadzinika avambane ndi ana a Amoni. 12Ndipo anati, Akandilaka
Aaramu, udzandilanditsa ndiwe; koma akakulaka ana a Amoni,
ndidzakulanditsa ndine. 13Limbika mtima, tilimbikire anthu athu,
ndi midzi ya Mulungu wathu; ndipo Yehova acite
comkomera. 14Pamenepo Yoabu ndi anthu anali naye anayandikira
pamaso pa Aaramu kulimbana nao, ndipo anawathawa. 15Ndipo
pakuona ana a Amoni kuti adathawa Aaramu, iwo omwe anathawa
pamaso pa Abisai mbale wace, nalowa m'mudzi. Pamenepo Yoabu
anadza ku Yerusalemu. 16Ndipo pakuona Aaramu kuti Israyeli
anawakantha, anatumiza mithenga, naturuka nao Aaramu
akukhala tsidya lija la mtsinjewo; ndi Sofaki kazembe wa khamu la
Hadarezeri anawatsogolera. 17Ndipo anamuuza Davide; namemeza
iye Aisrayeli onse, naoloka Yordano, nawadzera, nanika nkhondo

ayambane nao. Atandandalitsa nkhondo Davide kuyambana ndi
Aaramu, anaponyana naye. 18Ndipo Aaramu anathawa pamaso pa
Israyeli; ndipo Davide anapha Aaramu apamagareta zikwi zisanu
ndi ziwiri, ndi oyenda pansi zikwi makumi anai; napha Sofaki
kazembe wa khamulo. 19Ndipo pakuona anyamata a Hadarezeri
kuti Israyeli anawakantha, anapangana mtendere ndi Davide,
namtumikira; ndi Aaramu anakana kuthandizanso ana a Amoni.

©The Bible Society of Malawi, 1992

1Ndipo kunali, pofikanso caka, nyengo yakuturuka mafumu, Yoabu
anatsogolera khamu lamphamvu, napasula dziko la ana a Amoni,
nadza, naumangira misasa Raba. Koma Davide anakhala ku
Yerusalemu. Ndipo Yoabu anakantha Raba, naupasula. 2Ndipo
Davide anatenga korona wa mfumu yao kumcotsa pamutu pace,
napeza kulemera kwace talente wa golidi; panalinso miyala ya
mtengo wace pamenepo; ndipo anamuika pamutu pa Davide,
naturutsa zankhondo za m'mudzimo zambiri ndithu. 3Naturutsanso
anthu anali m'mwemo, nawaceka ndi mipeni ya mana mano, ndi
zipangizo zocekera zacitsulo, ndi nkhwangwa. Anatero Davide ndi
midzi yonse ya ana a Amoni. Ndipo Davide ndi anthu onse
anabwera ku Yerusalemu.

Abwereza kukantha Afilisti

4Ndipo zitatha izi, inauka nkhondo ku Gezeri ndi Afilisti; pamenepo
Sibekai Mhusati anapha Sipai wa ana a cimphona; ndipo
anawagonjetsa. 5Ndipo panalinso nkhondo ndi Afgisti; ndi Elihanani
mwana wa Yairi anapha Lami mbale wa Goliati Mgiti, amene luti la
mkondo wace linanga mtanda woombera nsaru. 6Ndipo panalinso
nkhondo ku Gati; kumeneko kunali munthu wa msinkhu waukuru,
amene zala zace za kumanja ndi kumapazi ndizo makumi awiri
mphambu zinai; zisanu ndi cimodzi ku dzanja liri lonse, ndi zisanu
ndi cimodzi ku phazi liri lonse; nayenso anabadwa mwa
cimphonaco. 7Ndipo potonza Israyeli iyeyu Yonatani mwana wa
Simeya mbale wace wa Davide anamkantha. 8Awa anabadwa mwa
cimphonaco ku Gati, koma anagwa ndi dzanja la Davide ndi la
anyamata ace.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Davide awerenga anthu; mliri ugwera Israyeli

1Pamenepo Satana anaukira Israyeli, nasonkhezera Davide
awerenge Israyeli. 2Ndipo Davide anati kwa Yoabu ndi kwa akuru a
anthu, Kawerengeni Israyeli kuyambira ku Beereseba kufikira ku
Dani; nimundibwezere mau, kuti ndidziwe ciwerengo cao. 3Nati
Yoabu, Yehova aonjezere pa anthu ace monga ali kazana; koma,
mbuyanga mfumu, sali onse anyamata akapolo a mbuyanga?
nanga afuniranji cinthuci mbuyanga, adzaparamulitsa Israyeli
bwanji? 4Koma mau a mfumu anamlaka Yoabu. Naturuka Yoabu,
nakayendayenda mwa Aisrayeli onse, nadza ku Yerusalemu. 5Ndipo
Yoabu anapereka kwa Davide ciwerengo ca anthu owerengedwa.
Ndipo Aisrayeli onse anali zikwi mazana khumi ndi limodzi osolola
lupanga, ndi Yuda anali zikwi mazana anai mphambu makumi
asanu ndi awiri akusolola lupanga, 6Koma sanawerenga Alevi ndi
Abenjamini pakati pao; pakuti mau a mfumu anamnyansira
Yoabu. 7Ndipo Mulungu anaipidwa naco cinthuci, cifukwa cace iye
anakantha Israyeli. 8Pamenepo Davide anati kwa Mulungu,
Ndacimwa kwakukuru ndi kucita cinthu ici; koma tsopano, mucotse
mphulupulu ya kapolo wanu, pakuti ndacita kopusa ndithu. 9Ndipo
Yehova ananena ndi Gadi mlauli wa Davide, ndi kuti, 10Kanene kwa
Davide kuti, Atero Yehova, Ndikuikira zitatu; dzisankhireko cimodzi
ndikucitire ici. 11Nadza Gadi kwa Davide, nanena naye, Atero
Yehova, Dzitengereko; 12kapena zaka zitatu za njala; kapena
miyezi itatu ya kuthedwa pamaso pa adani ako, ndi kuti lupanga la
adani ako likupeze; kapena masiku atatu lupanga la Yehova, ndilo
mliri m'dzikomo, ndi mthenga wakuononga wa Yehova mwa malire
onse a Israyeli, Ulingirire tsono, ndimbwezere mau anji iye amene
ananditume ine? 13Ndipo Davide anati kwa Gadi, Ndipsinjika
kwambiri; ndigwere m'dzanja la Yehova, pakuti zifundo zace
zicurukadi; koma ndisagwere m'dzanja la munthu. 14Momwemo
Yehova anatumiza mliri pa Israyeli; ndipo adagwapo amuna zikwi
makumi asanu ndi awiri a Israyeli.

Davide amangira Yehova guwa la nsembe pa dwale la Orinani

15Ndipo Mulungu anatuma mthenga ku Yerusalemu kuuononga;
ndipo poti auononge, Yehova anapenya, naleka coipaci; nati kwa
mthenga wakuononga, Cakwanira, bweza dzanja lako tsopano. Ndi
mthenga wa Yehova anaima pa dwale la Orinani Myebusi, 16Ndipo
Davide anakweza maso ace, naona mthenga wa Yehova alikuima
pakati pa dziko ndi thambo, ali nalo lupanga losolola m'dzanja
lace, lotambasukira pa Yerusalemu. Pamenepo Davide ndi akuru
obvala ziguduli anagwa nkhope zao pansi. 17Ndipo Davide anati
kwa Mulungu, Si ndine nanga ndalamulira kuti awerenge anthu?

Inde, ndine amene ndacimwa ndi kucita coipa ndithu; koma nkhosa izi zinacitanji? dzanja lanu, Yehova Mulungu wanga, Gnditsutse ine ndi nyumba ya atate wanga, koma Gsatsutse anthu anu ndi kuwacitira mliri. 18Pamenepo mthenga wa Yehova anauza Gadi kuti anene ndi Davide, akwere Davideyo kuutsira Yehova guwa la nsembe pa dwale la Orinani Myebusi, 19Ndipo Davide anakwera monga mwa mau a Gadi adawanena m'dzina la Yehova. 20Poceuka Orinani anaona wamthengayo; ndi ana ace amuna anai anali naye anabisala. Koma Orinani analikupuntha tirigu. 21Ndipo pofika Davide kwa Orinani, Orinaniyo anapenyetsa, naona Davide, naturuka kudwale, nawerama kwa Davide, nkhope yace pansi. 22Davide tsono anati kwa Orinani, Ndipatse padwale pano kuti ndimangepo guwa la nsembe la Yehova; undipatse gi pa mtengo wace wonse, kuti mliri ulekeke pa anthu. 23Ndipo Orinani anati kwa Davide, Mulitenge, ndi mbuye wanga mfumu icite comkomera m'maso mwace; taonani, ndikupatsani ng'ombe za nsembe zopsereza; ndi zipangizo zopunthira zikhale nkhuni, ndi tirigu wa nsembe yaufa; ndizipereka zonse. 24Koma mfumu Davide anati kwa Orinani, lai, koma ndidzaligula pa mtengo wace wonse; pakuti sindidzatengera Yehova ciri cako, kapena kupereka nsembe yopsereza yopanda mtengo wace. 25Momwemo Davide anapatsa Orinani cogulira malowa golidi wa masekeli mazana asanu ndi limodzi kulemera kwace. 26Ndipo Davide anamangira Yehova guwa la nsembe komweko; napereka nsembe zopsereza, ndi nsembe zoyamika, naitana kwa Yehova; ndipo anamyankha ali m'Mwamba ndi mota pa guwa la nsembe yopsereza. 27Ndipo Yehova anauza wamthenga kuti abweze lupanga lace m'cimace.
28Nthawi yomweyi, pakuona Davide kuti Yehova anambvomereza pa dwale la Orinani Myebusi, anaphera nsembe pomwepo. 29Pakuti kacisi wa Yehova amene Mose anapanga m'cipululu, ndi guwa la nsembe yopsereza, zinali pa msanje wa ku Gibeoni nthawi yomweyi. 30Kama Davide sanathe kumuka kukhomo kwace kufunsira kwa Mulungu, pakuti anaopa lupanga la mthenga wa Yehova.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Davide akonzeratu mirimo yakumanga kacisi

1Ndipo Davide anati, Pano padzakhala nyumba ya Yehova
Mulungu, ndi pano padzakhala guwa la nsembe yopsereza la
Israyeli.
2Ndipo Davide anati asonkhanitse alendo okhala m'dziko la
Israyeli; iye naika osema miyala afukule miyala, aiseme kuti
amange nayo nyumba ya Mulungu. 3Nakonzeratu Davide citsulo
cocuruka ca misomali ya ku zitseko za zipata, ndi ya kuphatikizitsa;
ndi mkuwa wocuruka wosauyesa kulemera kwace; 4ndi mitengo
yamikungudza yosaiwerenga; pakuti Asidoni ndi Aturo anabwera
nayo kwa Davide mitengo yamikungudza yocuruka, 5Ndipo Davide
anati, Solomo mwana wanga ndiye mnyamata ndi wosakwima, ndi
nyumba imene adzaimangira Yehova ikhale yaikuru yopambana,
yomveka ndi ya ulemerero mwa maiko onse; ndiikonzeretu mirimo.
Momwemo Davide anakonzeratu mocuruka asanamwalire.

Davide amlangiza Solomo ammangire Yehova nyumba

6Pamenepo iye anaitana Solomo mwana wace, namlangiza
ammangire Yehova Mulungu wa Israyeli nyumba. 7Ndipo Davide
anati kwa Solomo mwana wace, Kunena za ine, kumtima kwanga
kudati, ndilimangire dzina la Yehova Mulungu wanga
nyumba. 8Koma mau a Yehova anandidzera, kuti, Wakhetsa mwazi
wocuruka, popeza wacita nkhondo zazikuru; sudzamangira dzina
langa nyumba, popeza wakhetsa pansi mwazi wambiri pamaso
panga; 9taona, udzabala mwana, ndiye adzakhala munthu wa phe;
ndipo nelidzampumulitsira adani ace onse pozungulirapo, pakuti
dzina lace lidzakhala Solomo; ndipo ndidzapatsa Israyeli mtendere
ndi bata masiku ace; 10iyeyu adzamangira dzina langa nyumba;
iye adzakhala mwana wanga, ndi Ine ndidzakhala Atate wace;
ndipo ndidzakhazikitsa mpando wacifumu wa ufumu wace pa
Israyeli kosalekeza. 11Tsono, mwana wanga, Yehova akhale nawe;
nulemerere, numange nyumba ya Yehova Mulungu wako monga
ananena za iwe. 12Cokhaci, Yehova akupatse nzeru ndi luntha,
nakulangize za Israyeli, kuti usunge cilamulo ca Yehova Mulungu
wako, 13Momwemo udzalemerera, ukasamalira kucita malemba ndi
maweruzo amene Yehova analangiza Mose za Israyeli; limbikatu,
nulimbike mtima, usaope, usade mtima. 14Taona tsono,
m'kuzunzika kwanga ndinakonzeratu nyumba ya Yehova matalente
zikwi zana limodzi a golidi, ndi matalente zikwi zikwi a siliva, ndi
mkuwa, ndi citsulo, osayesa kulemera kwace, pakuti zidacurukaeli;
mitengo yomwe ndi miyala ndakonzeratu; nuonjezereko. 15Uli
naonso anchito ocuruka ofukula miyala, ndi amisiri a miyala ndi a
mitengo, ndi amuna onse aluso akucita nchito ziri zonse; 16golidi,
ndi siliva, ndi mkuwa, ndi citsulo, nzosawerengeka; nyamuka,

nucite, Yehova akhale nawe. 17Davide analangizanso akalonga a
Israyeli athanelize Solomo mwana wace, ndi kuti, 18Kodi Yehova
Mulungu wanu sali nanu? sanakupumulitsani pambali ponse?
pakuti anapereka nzika za m'dziko m'dzanja mwanga, ndi dziko
lagonjetsedwa pamaso pa Yehova, ndi pamaso pa anthu
ace. 19Perekani tsono mtima ndi moyo wanu kufunafuna Yehova
Mulungu wanu; ndipo nyamukani ndi kumanga malo opatulika a
Yehova Mulungu, kuti abwere nalo likasa la cipangano la Yehova,
ndi zipangizo zopatulika za Mulungu, ku nyumba imene
idzamangidwira dzina la Yehova.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Davide alonga Solomo m'ufumu, nakonza cigawo ca Alevi

1Atakalamba tsono Davide ndi kucuruka masiku, iye analonga
mwana wace Solomo akhale mfumu ya Israyeli. 2Ndipo
anasonkhanitsa akuru onse a Israyeli, ndi ansembe ndi
Alevi. 3Ndipo anawerengedwa Alevi oyambira zaka makumi atatu
ndi mphambu, ndipo ciwerengo cao kuwawerenga mmodzi mmodzi
ndico amuna zikwi makumi atatu mphambu zisanu ndi zitatu. 4A
iwowa zikwi makumi awiri mphambu zinai anayang'anira nchito ya
nyumba ya Yehova, ndi zikwi zisanu ndi cimodzi ndiwo akapitao ndi
oweruza, 5ndi zikwi zinai odikira; ndi zikwi zinai analemekeza
Yehova ndi zoyimbira zimene ndinazipanga, anati Davide, kuti
alemekeze nazo. 6Ndipo Davide anawagawa magawo monga mwa
ana a Levi: Gerisomu, Kohati, ndi Merari. 7A Agerisomu: Ladani ndi
Simeyi, 8Ana a Ladani: wamkuru ndi Yehieli, ndi Zethamu, ndi Yoeli;
atatu. 9Ana a Simeyi: Selomoti, ndi Hazieli, ndi Hanani; atatu.
Ndiwo akuru a nyumba za makolo a Ladani. 10Ndi ana a Simeyi:
Yahati, Zina, ndi Yeusi, ndi Beriya. Awa anai ndiwo ana a
Simeyi. 11Wamkuru wa iwo ndi Yahati, mnzace ndi Ziza; koma Yeusi
ndi Beriya analibe ana ambiri, potero anakhala nyumba ya kholo
yowerengedwa pamodzi. 12Ana a Kohati: Amiramu, Izara, Hebroni,
ndi Uzieli; anai. 13Ana a Amiramu: Aroni, ndi Mose; ndipo Aroni
anasankhidwa kuti apatule zopatulikitsa, iye ndi ana ace,
kosalekeza, kufukiza pamaso pa Yehova, kumtumikira, ndi
kudalitsa m'dzina lace kosatha. 14Kunena za Mose munthu wa
Mulunguyo, ana ace anaehulidwa mwa pfuko la Levi. 15Ana a Mose:
Gerisomu, ndi Eliezeri. 16Ana a Gerisomu: wamkuru ndi
Sebuyeli. 17Ndi ana a Eliezeri: wamkuru ndi Rehabiya. Ndipo
Eliezeri analibe ana ena, koma ana a Rehabiya anacuruka
kwambiri. 18Ana a Izara: wamkuru ndiye Selomiti. 19Ana a Hebroni:
wamkuru ndi Yeriya, waciwiri ndi Amariya, wacitatu ndi Yehazieli,
wacinai ndi Yekameamu, 20Ana a Uzieli: wamkuru ndi Mika,
waciwiri ndi Isiya. 21Ana a Merari: Mali ndi Musi. Ndi ana a Mali:
Eleazara ndi Kisi. 22Nafa Eleazara wopanda ana amuna, koma ana
akazi ndiwo; ndi asuweni ao ana a Kisi anawatenga akhale akazi
ao. 23Ana a Musi: Mali, ndi Ederi, ndi Yeremoti; atatu. 24Awa ndi
ana a Levi monga mwa nyumba za makolo ao, ndiwo akuru a
nyumba za makolo a iwo owerengedwa mwa ciwerengo ca maina
mmodzi mmodzi, akugwira nchito ya utumiki wa nyumba ya
Yehova, kuyambira a zaka makumi awiri ndi mphambu. 25Pakuti
Davide anati, Yehova Mulungu wa Israyeli wapumulitsa anthu ace;
ndipo akhala m'Yerusalemu kosatha; 26ndiponso Alevi asasenzenso
kacisi ndi zipangizo zace zonse za utumiki wace. 27Pakuti monga
mwa mau ace otsiriza a Davide, ana a Levi anawerengedwa

kuyambira a zaka makumi awiri ndi mphambu. 28Pakuti nchito yao
ndiyo kuimirira ana a Aroni, atumikire m'nyumba ya Yehova,
m'mabwalo, ndi kuzipinda, ndi kuyeretsa zopatulika zonse; inde
nchito za utumiki wa nyumba ya Mulungu; 29ya mkate woonekera
womwe, ndi ya ufa wosalala wa nsembe yaufa, ndi ya timitanda
taphanthiphanthi topanda cotupitsa, ndi ya ciwaya, ndi
yakukazinga, ndi ya miyeso iri yonse; 30ndi kuimirira m'mawa ndi
m'mawa kuyamika ndi kulemekeza Yehova, momwemonso
madzulo; 31ndi kupereka nsembe zopsereza zonse kwa Yehova, za
masabata, za pokhala mwezi, za nyengo zoikika, kuwerenga kwace
monga mwa lemba lace, kosalekeza pamaso pa Yehova; 32ndi kuti
asunge udikiro wa cihema cokomanako, ndi udikiro wa malo
opatulika ndi udikiro wa ana a Aroni abale ao, potumikira nyumba
ya Yehova.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Magawo 24 a ansembe

1Ndipo magawidwe a ana a Aroni ndi awa. Ana a Aroni: Nadabu,
ndi Abihu, Eleazara, ndi Itamara. 2Koma Nadabu ndi Abihu anafa,
atate wao akali ndi moyo, opanda ana; momwemo Eleazara ndi
Itamara anacita nchito ya nsembe. 3Ndipo Davide pamodzi ndi
Zadoki wa ana a Eleazara, ndi Ahimeleke wa ana a Itamara,
anawagawa, monga mwa malongosoledwe ao m'utumiki
wao. 4Ndipo anapeza kuti amuna akuru a ana a Eleazara
anacuruka, a ana a Itamara anacepa; nawagawa motero: pa ana a
Eleazara panali khumi mphambu asanu ndi mmodzi, akuru a
nyumba za makolo; ndi pa ana a Itamara, monga mwa nyumba za
makolo ao, panali asanu ndi atatu. 5Ndipo anawagawa ndi maere,
awa ndi aja; pakuti panali akalonga a malo opatulika, ndi akalonga
a kwa Mulungu, a ana a Eleazara ndi a ana a Itamara omwe. 6Ndi
Semaya mwana wa Netaneli mlembi, ndiye wa Alevi,
anawalembera pamaso pa mfumu; ndi akalonga, ndi Zadoki
wansembe, ndi Ahimeleke mwana wa Abyatara, a akuru a nyumba
za makolo a ansembe ndi Alevi, anatenga nyumba imodzi ya kholo
lace ya Eleazara, ndi imodzi ya Itamara. 7Ndipo maere oyamba
anamgwera Yehoyaribu, waciwiri Yedaya, 8wacitatu Harimu,
wacinai Seorimu, 9wacisanu Malikiya, wacisanu ndi cimodzi
Miyamini, 10wacisanu ndi ciwiri Hakozi, wacisanu ndi citatu
Abiya, 11wacisanu ndi cinai Yesuwa, wakhumi Sekaniya, 12wakhumi
ndi cimodzi Eliyasibu, wakhumi ndi ciwiri Yakimu, 13wakhumi ndi
citatu Hupa, wakhumi ndi cinai Yesebeabu, 14wakhumi ndi cisanu
Biliga, wakhumi ndi cisanu ndi cimodzi Imeri, 15wakhumi ndi cisanu
ndi ciwiri Heziri, wakhumi ndi cisanu ndi citatu
Hapizezi, 16wakhumi ndi cisanu ndi cinai Petahiya, wa makumi
awiri Yehezikeli, 17wa makumi awiri ndi cimodzi Yakini, wa makumi
awiri ndi ciwiri Gamuli, 18wa makumi awiri ndi citatu Delaya, wa
makumi awiri ndi cinai Miziya. 19Awa ndi malongosoledwe ao
m'utumiki wao kulowa m'nyumba ya Yehova, monga mwa ciweruzo
adawapatsa Aroni atate wao, monga Yehova Mulungu wa Israyeli
anamlamulira.
20Ndipo wa ana otsala a Levi: wa ana a Amiramu, Subaeli; wa ana
a Subaeli, Yedeya. 21Wa Rehabiya: wa ana a Rehabiya, mkuru ndi
Isiya. 22Wa Aizari: Selomoti; wa ana a Selomoti, Yahati. 23Ndi wa
ana a Hebroni: mkuru ndi Yeriya, waciwiri Amariya, wacitatu
Yahazieli, wacinai Yekameamu. 24Wa ana a Uziyeli, Mika; wa ana a
Mika, Samiri. 25Mbale wa Mika, Isiya; a ana a Isiya, Zekariya, 26Ana
a Merari: Mali ndi Musi; mwana wa Yaziya, Beno. 27Ana a Merari:
wa Yaziya, Beno, ndi Sohamu, ndi Sakuri, ndi Ibri. 28Wa Mali:
Eleazara, ndiye wopanda ana. 29Wa Kisi: mwana wa Kisi,

Yerameli. 30Ndi ana a Musi: Mali, ndi Ederi, ndi Yerimoti, Awa ndi
ana a Alevi monga mwa nyumba za makolo ao. 31Awanso anacita
maere monga abale ao ana a Aroni, pamaso pa Davide mfumu, ndi
Zadoki, ndi Ahimeleki, ndi akuru a nyumba za makolo za ansembe
ndi Alevi; mkuru wa nyumba za makolo monga mng'ono wace.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Cigawo ca oyimbira nyimbo

1Ndipo Davide ndi akazembe a gulu la nkhondo anapatulira
utumikiwo ena a ana a Asafu, ndi a Hemani, ndi a Yedutuni,
anenere ndi azeze, ndi zisakasa, ndi nsanje; ndi ciwerengo ca
anchito monga mwa kutumikira kwao ndko: 2a ana a Asafu: Zakuri,
ndi Yosefe, ndi Netaniya, ndi Asarela, ana a Asafu; mwa cilangizo
ca Asafu, wakunenera mwa cilangizo ca mfumu. 3A Yedntuni, ana a
Yedutuni: Gedaliya, ndi Zeri, ndi Yesaya, Hasabiya, ndi Matitiya,
asanu ndi mmodzi; mwa cilangizo ca atate wao Yedutuni, ndiye
wakunenera ndi kuyamika ndi kulemekeza Yehova ndi zeze. 4A
Hemani, ana a Hemani: Bukiya, Mataniya, Uziyeli, Sebuyeli, ndi
Yerimoti, Hananiya, Hanani, Eliyata, Gidaliti, ndi Romamti-Ezeri,
Yosibekasa, Maloti, Hotiri, Mahazioti; 5awa onse ndiwo ana a
Hemani mlauli wa mfumu m'mau a Mulungu, kuti akweze
mphamvu yace. Ndipo Mulungu anapatsa Hemani ana amuna
khumi ndi anai, ndi ana akazi atatu. 6Onsewa anawalangiza ndi
atate wao ayimbe m'nyumba ya Yehova ndi nsanje, zisakasa ndi
azeze; atumikire nazo m'nyumba ya Mulungu; ndipo Asafu,
Yedutuni, ndi Hemani, anawalangiza ndi mfumu. 7Ndipo ciwerengo
cao, pamodzi ndi abale ao ophunzitsidwa ayimbire Yehova, onse
anthetemya, ndiwo mazana awiri mphambu makumi asanu ndi
atatu. 8Ndipo anacita maere pa udikiro wao, analingana onse,
ang'ono ndi akuru, mphunzitsi ndi wophunzira. 9Maere oyamba
tsono anagwera a banja la Asafu ndiye Yosefe; waciwiri Gedaliya,
iye ndi abale ace, ndi ana ace khumi ndi awiri; 10wacitatu Zakuri,
ana ace ndi abale ace khumi ndi awiri; 11wacinai Izri, ana ace ndi
abale ace khumi ndi awiri; 12wacisanu Netaniya, ana ace ndi abale
ace khumi ndi awiri; 13wacisanu ndi cimodzi Bukiya, ana ace ndi
abale ace khumi ndi awiri; 14wacisanu ndi ciwiri Yesarela: ana ace
ndi abale ace khumi ndi awiri; 15wacisanu ndi citatu Yesaya, ana
ace ndi abale ace khumi ndi awiri; 16wacisanu ndi cinai Mataniya,
ana ace ndi abale ace khumi ndi awiri: 17wakhumi Simeyi, ana ace
ndi abale ace khumi ndi awiri; 18wakhumi ndi cimodzi Azareli, ana
ace ndi abale ace khumi ndi awiri; 19wakhumi ndi ciwiri Hasabiya,
ana ace ndi abale ace khumi ndi awiri; 20wakhumi ndi citatu
Subaeli, ana ace ndi abale ace khumi ndi awiri; 21wakhumi ndi
cinai Matitiya, ana ace ndi abale ace khumi ndi awiri; 22wakhumi
ndi cisanu Yeremoti, ana ace ndi abale ace khumi ndi
awiri; 23wakhumi ndi cisanu ndi cimodzi Hananiya, ana ace ndi
abale ace khumi ndi awiri; 24wakhumi ndi cisanu ndi ciwiri
Yosibekasa, ana ace ndi abale ace khumi ndi awiri; 25wakhumi ndi
cisanu ndi citatu Hanani, ana ace ndi abale ace khumi ndi
awiri; 26wakhumi ndi cisanu ndi cinai Maloti, ana ace ndi abale ace

khumi ndi awiri; 27wa makumi awiri Eliyata, ana ace ndi abale ace khumi ndi awiri; 28wa makumi awiri ndi cimodzi Hotiri, ana ace ndi abale ace khumi ndi awiri; 29wa makumi awiri ndi ciwiri Gidaliti, ana ace ndi abale ace khumi ndi awiri; 30wa makumi awiri ndi citatu Mahazioti, ana ace ndi abale ace khumi ndi awiri; 31wa makumi awiri ndi cinai RomamtiEzeri, ana ace ndi abale ace khumi ndi awiri.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Cigawo ca odikira

1A magawidwe a odikira a Akora: Meselemiya mwana wa Kore wa
ana a Asafu. 2Ndipo Meselemiya anali ndi ana, woyamba Zekariya,
waciwiri Yedyaeli, wacitatu Zebadiya, wacinai Yatiniyeli, 3wacisanu
Elamu, wacisanu ndi cimodzi Yohanana, wacisanu ndi ciwiri
Elihunai. 4Ndipo Obedi Edomu anali nao ana, woyamba Semaya,
waciwiri Yozabadi, wacitatu Yowa, wacinai Sakara, wacisanu
Netaneli, 5wacisanu ndi cimodzi Amiyeli, wacisanu ndi ciwiri
Isakara, wacisanu ndi citatu Peuletai; pakuti Mulungu
adamdalitsa. 6Kwa Semaya mwana wace yemwe kunabadwa ana,
akulamulira nyumba ya atate wao; pakuti anali ngwazi
zamphamvu. 7Ana a Semaya: Otini, ndi Refaeli, ndi Obedi,
Elzabadi, amene abale ao ndiwo odziwa mphamvu, Elihu, ndi
Semakiya. 8Onsewa ndiwo a ana a Obedi Edomu; iwo ndi ana ao,
ndi abale ao, anthu odziwa mphamvu yakutumikira, makumi asanu
ndi limodzi mphambu awiri a Obedi Edomu. 9Ndi Meselemiya anali
ndi ana, ndi abale odziwa mphamvu khumi mphambu asanu ndi
atatu. 10Hosa yemwe wa ana a Merari anali ndi ana, wamkuru ndi
Simri; pakuti ngakhale sanali wobadwa woyamba, atate wace
anamuyesa wamkuru; 11waciwiri Hilikiya, wacitatu Tebaliya,
wacinai Zekariya; ana ndi abale onse a Hosa ndiwo khumi ndi
atatu. 12Mwa iwowa munali magawidwe a odikira, mwa akulu a
amuna akucita udikiro wao, monga abale ao, kutumikira m'nyumba
ya Yehova. 13Ndipo anacita maere ang'ono ndi akuru, monga mwa
nyumba za makolo ao, kucitira zipata zonse. 14Ndi maere a
kum'mawa anagwera Selemiya. Ndipo anacitira maere Zekariya
mwana wace, phungu wanzeru, ndi maere anamgwera
kumpoto; 15Obedi Edomu kumwela, ndi ana ace nyumba ya
akatundu. 16Supimu ndi Hosa kumadzulo, ku cipata ca Saleketi, ku
mseu wokwerapo, udikiro pandunji pa udikiro. 17Kum'mawa kunali
Alevi asanu ndi mmodzi, kumpoto anai tsiku ndi tsiku, kumwela
anai tsiku ndi tsiku, ndi a nyumba ya akatundu awiri ndi awiri. 18Ku
Parabara kumadzulo anai kumseu, ndi awiri ku Parabara. 19Awa ndi
magawidwe a odikira; a ana a Akora, ndi a ana a Merari.

Osunga cuma ca Nyumba ya Mulungu

20Ndipo wa Alevi, Ahiya anayang'anira cuma ca nyumba ya
Mulungu, ndi cuma ca zopatulika. 21Ana a Ladani: ana a Ladani a
Agerisoni, akuru a nyumba za makolo a Ladani Mgerisoni,
Yehieli. 22Ana a Yehieli: Zetamu ndi Yoeli mbale wace, oyang'anira
cuma ca nyumba ya Yehova. 23A Amirami, a Aizari, a Ahebroni, a
Auziyeli; 24ndi Sebueli mwana wa Gerisomu, mwana wa Mose,
ndiye mkuru woyang'anira zuma. 25Ndi abale ace a Eliezeri:
Rehabiya mwana wace, ndi Yesava mwana wace ndi Yorramu

mwana wace, ndi Zikiri mwana wace, ndi Selomoti mwana wace. 26Selomoti amene ndi abale ace anayang'anira cuma conse ca zinthu zopatulika, zimene Davide mfumu ndi akuru a nyumba za akulu, akuru a zikwi ndi mazana, adazipatula. 27Kutenga pa zofunkha kunkhondo, anapatulako kukonzera nyumba ya Yehova. 28Ndipo zonse adazipatula Samueli mlauli, ndi Sauli mwana wa Kisi, ndi Abineri mwana wa Neri, ndi Yoabu mwana wa Zeruya; ali yense anapatula kanthu kali konse, anazisunga Selomoti ndi abale ace.

Akapitao ndi oweruza

29A Aizara: Kenaniya ndi ana ace anacita nchito ya pabwalo ya Israyeli, akapitao ndi oweruza mirandu. 30A Ahebroni: Hasabiya ndi abale ace odziwa mphamvu cikwi cimodzi mphambu mazana asanu ndi awiri anayang'anira Israyeli tsidya lino la Yordano kumadzulo, kuyang'anira nchito yonse ya Yehova, ndi kutumikira mfumu. 31Yeriya ndiye mkuru wa Ahebroni, wa Ahebroni monga mwa mibadwo ya nyumba za makolo. Caka ca makumi anai ca ufumu wa Davide anafunafuna, napeza mwa iwowa ngwazi zamphamvu ku Yazeri wa ku Gileadi. 32Ndi abale ace ngwazi ndiwo zikwi ziwiri mphambu mazana asanu ndi awiri, akuru a nyumba za makolo, amene mfumu Davide anaika akhale oyang'anira a Arubeni, ndi Agadi, ndi pfuko la Manase logawika pakati, pa zinthu zonse za Mulungu ndi zinthu za mfumu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Ankhondo ndi akazembe ao

1Ndipo ana a Israyeli monga mwa ciwerengo cao, kunena za akuru
a nyumba za makolo ao, ndi akazembe a zikwi, ndi a mazana, ndi
akapitao ao akutumikira mfumu mu nchito iri yonse ya
magawidwe, akulowa ndi kuturuka mwezi ndi mwezi, miyezi yonse
ya caka, cigawo ciri conse nca amuna zikwi makumi awiri
mphambu zinai. 2Woyang'anira cigawo coyamba ca mwezi,
woyamba ndiye Yasobeamu mwana wa Zabidiyeli; m'cigawo
mwace munali zikwi makumi awiri mphambu zinai. 3Ndiye wa ana
a Perezi, mkuru wa akazembe onse a khamu mwezi
woyamba. 4Woyang'anira cigawo ca mwezi waciwiri ndiye Dodai M-
ahohi ndi cigawo cace; ndi Mikiloti mtsogoleri, ndi m'cigawo cace
munali zikwi makumi awiri mphambu zinai. 5Kazembe wacitatu wa
khamu wa mwezi wacitatu ndiye Benaya mwana wa Yehoyada
wansembe wamkuru; ndi m'cigawo mwacemunalinso zikwi makumi
awiri mphambu zinai. 6Benaya ameneyo ndiye wamphamvu uja wa
makumi atatu aja, woyang'anira makumi atatu aja; woyang'anira
cigawo cace ndi Amizabadi mwana wace. 7Wacinai wa mwezi
wacinai ndiye Asebeli mbale wa Yoabu, ndi pambuyo pace
Zebadiya mwana wace; ndi m'cigawo mwace munali zikwi makumi
awiri mphambu zinai. 8Kazembe wacisanu wa mwezi wacisanu
ndiye Samuti M-izra; ndi m'cigawo mwace zikwi makumi awiri
mphambu zinai. 9Wacisanu ndi cimodzi wa mwezi wacisanu ndi
cimodzi ndiye Ira mwana wa Ikesi Mtekoi; ndi m'cigawo mwace
zikwi makumi awiri mphambu zinai. 10Wacisanu ndi ciwiri wa
mwezi wacisanu ndi ciwiri ndiye Helezi Mpeloni wa ana a Efraimu;
ndi m'cigawo mwace zikwi makumi awiri mphambu
zinai. 11Wacisanu ndi citatu wa mwezi wacisanu ndi citatu ndiye
Sibekai Mhusati wa Afera; ndi m'cigawo mwace zikwi makumi awiri
mphambu zinai. 12Wacisanu ndi cinai wa mwezi wacisanu ndi cinai
ndiye Abiezeri M-anatoti wa Abenjamini; ndi m'cigawo mwace zikwi
makumi awiri mphambu zinai. 13Wakhumi wa mwezi wakhumi
ndiye Maharai Mnetofati wa Azera; ndi m'cigawo mwace zikwi
makumi awiri mphambu zinai. 14Wakhumi ndi cimodzi wa mwezi
wakhumi ndi cimodzi ndiye Benaya Mpiratoni wa ana a Efraimu;
ndi m'cigawo mwace zikwi makumi awiri mphambu
zinai. 15Wakhumi ndi ciwiri wa mwezi wakhumi ndi ciwiri ndiye
Heledai Mnetofati wa Otiniyeli; ndi m'cigawo mwace zikwi makumi
awiri mphambu zinai.

Oyang'anira mafuko 12 a Israyeli

16Koma oyang'anira mafuko a lsrayeli ndi awa: wa Arubeni
mtsogoleri wao ndiye Eliezeri mwana wa Zikiri; wa Asimeoni,
Sefatiya mwana wa Maaka; 17wa Alevi, Hasabiya mwana wa

Kemueli; wa Aroni, Zadoki; 18wa Yuda, Elihu mbale wina wa Davide;
wa Isakara, Omri mwana wa Mikaeli; 19wa Zebuluni, Isimaya
mwana wa Obadiya; wa Nafitali, Yeremoti mwana wa Azrieli; 20wa
ana a Efraimu, Hoseya mwana wa Azaziya; wa pfuko la Manase
logawika pakati, Yoeli mwana wa Pedaya; 21wa pfuko la Manase
logawika pakati m'Gileadi, Ido mwana wa Zekariya; wa Benjamini,
Yasiyeli mwana wa Abineri; 22wa Dani, Azareli mwana wa
Yerohamu. Awa ndi akazembe a mapfuko a Israyeli. 23Koma Davide
sanawerenga iwo a zaka makumi awiri ndi ocepapo, pakuti Yehova
adati kuti adzacurukitsa Israyeli ngati nyenyezi za
kuthambo. 24Yoabu mwana wa Zeruya anayamba kuwerenga,
koma sanatsiriza; ndi mkwiyo unagwera Israyeli cifukwa ca ici,
ndipo ciwerengo cao sicinalembedwa m'buku la mbiri ya mfumu
Davide.

Oyang'anira a zace za Davide

25Ndipo woyang'anira cuma ca mfumu ndiye Azimaveti mwana wa
Adiyeli, ndi woyang'anira wa cuma ca m'minda, m'mizinda ndi
m'miraga, ndi nyumba za nsanja, ndiye Yonatani mwana wa
Uziya; 26ndi woyang'anira iwo akugwira nchito ya m'munda
yakulima nthaka ndiye Ezri mwana wa Kelubi; 27ndi woyang'anira
minda yamphesa ndiye Simeyi Mramati; ndi woyang'anira zipatso
za minda yamphesa zisungike mosungiramo vinyo ndiye Zabidi
Msifimi; 28ndi woyang'anira mitengo yaazitona, ndi yamikuyu
yokhala kuzidikha kunsi, ndiye Baala Hanani Mgederi; ndi
woyang'anira zosungiramo mafuta ndiye Yoasi; 29ndi woyang'anira
ng'ombe zakudya m'Saroni ndiye Sitirai Msaroni; ndi woyang'anira
ng'ombe za m'zigwa ndiye Safabi mwana wa Adilai; 30ndi
woyang'anira ngamira ndiye Obili M-israyeli; ndi woyang'anira
aburu ndiye Yedeya Mmeronoti; 31ndi woyang'anira zoweta
zazing'ono ndiye Yazizi Mhagiri, Onsewa ndiwo akuru a zolemera
zace za Davide.

32Ndipo Yonatani atate wace wina wa Davide anali phungu,
munthu wanzeru ndi mlembi; ndi Yehieli mwana wa Hakimoni
anakhala ndi ana a mfumu; 33ndi Ahitofeli anali phungu wa mfumu,
ndi Husai M-ariki anali bwenzi la mfumu; 34ndi wotsatana ndi
Ahitofeli, Yehoyada mwana wa Benaya, ndi Abyatara; koma
kazembe wa nkhondo ya mfumu ndiye Yoabu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Davide alangiza akuru onse ndi Solomo yemwe

1Pamenepo Davide anasonkhanitsa ku Yerusalemu akalonga
Israyeli, a akalonga a mapfuko, ndi akuru a zigawo zakutumikira
mfumu, ndi akulu a zikwi, ndi akuru a mazana, ndi akuru a
zolemera zonse, ndi zoweta zonse za mfumu, ndi ana ace;
pamodzi ndi akapitao ndi anthu amphamvu, ndiwo ngwazi
zamphamvu onsewo. 2Ndipo mfumu Davide anaima ciriri, nati,
Mundimvere ine, abale anga ndi anthu anga, ine kumtima kwanga
ndinafuna kulimangira likasa la cipangano la Yehova, ndi
popondapo mapazi a Mulungu wathu nyumba yopumulira, ndipo
ndidakonzeratu za nyumbayi. 3Koma Mulungu anati kwa ine,
Sudzamangira dzina langa nyumba, popeza ndiwe munthu wa
nkhondo wokhetsa mwazi. 4Komatu Yehova Mulungu wa Israyeli
anasankha ine m'nyumba yonse ya atate wanga, ndikhale mfumu
ya Israyeli kosatha; pakuti anasankhiratu Yuda akhale mtsogoleri,
ndi m'nyumba ya Yuda nyumba ya atate wanga, ndi mwa ana a
atate wanga ndinamkomera ndine, andilonge ufumu wa Israyeli
yense; 5ndi mwa ana anga onse (pakuti Yehova wandipatsa ana
amuna ambiri), anasankha Solomo mwana wanga akhale pa
mpando wacifumu wa ufumu wa Yehova kuweruza Israyeli. 6Ndipo
anati kwa ine, Solomo mwana wako ndiye adzandimangira nyumba
yanga ndi mabwalo anga; pakuti ndamsankha akhale mwana
wanga, ndipo Ine ndidzakhala atate wace. 7Ndipo ndidzakhazikitsa
ufumu wace kosatha, akalimbika kucita malamulo anga ndi
maweruzo anga monga lero lino. 8Ndipo tsopano, pamaso pa
Aisrayeli onse, khamu la Yehova, ndi m'makutu a Mulungu wathu,
sungani, nimufunefune malamulo onse a Yehova Mulungu wanu,
kuti mukhale nalo lanu lanu dziko lokoma ili, ndi kulisiyira ana anu
pambuyo panu colowa cao kosalekeza. 9Ndipo iwe Solomo mwana
wanga, umdziwe Mulungu wa atate wako, umtumikire ndi mtima
wangwiro ndi moyo waufulu; pakuti Yehova asanthula mitima
yonse, nazindikira zolingirira zonse za maganizo; ukamfunafuna
iye udzampeza, koma ukamsiya iye adzakusiya kosatha. 10Cenjera
tsono, pakuti Yehova anakusankha iwe umange nyumba ya malo
opatulika; limbika, nucite.

Davide apereka kwa Solomo cifaniziro ndi mirimo ya Kacisi

11Pamenepo Davide anapatsa Solomo mwana wace cifaniziro ca
likole la kacisi, ndi ca nyumba zace, ndi ca zosungiramo cuma
zace, ndi ca zipinda zosanjikizana zace, ndi ca zipinda zace za
m'katimo, ndi ca kacisi wotetezerapo; 12ndi cifaniziro ca zonse
anali nazo mwa mzimu, ca mabwalo a nyumba ya Yehova, ndi ca
zipinda zonse pozungulirapo, ca zosungiramo cuma za nyumba ya
Mulungu, ndi ca zosungiramo cuma za zinthu zopatulika; 13ndi ca

magawidwe a ansembe ndi Alevi, ndi ca nchito zonse za utumiki
wa nyumba ya Yehova, ndi ca zipangizo za utumiki wa nyumba ya
Yehova; 14ca golidi woyesedwa kulemera kwace wa zipangizo
zagolidi, wa zipangizo zonse za nchito ya mtundu uli wonse; ca
siliva wa zipangizo zasiliva woyesedwa kulemera kwace, wa
zipangizo za nchito ya mitundu mitundu; 15mwa kulemera
kwacenso ca zoikapo nyali zagolidi, ndi nyali zace zagolidi, mwa
kulemera kwace ca coikapo nyali ciri conse, ndi nyali zace; ndi ca
zoikapo nyali zasiliva, siliva woyesedwa kulemera kwace wa
coikapo nyali ciri conse, ndi nyali zace, monga mwa coikapo nyali
ciri conse; 16ndi golidi woyesedwa kulemera kwace wa magome a
makate woonekera, wa gome liri lonse; ndi siliva wa magome
asiliva, 17ndi mitengo, ndi mbale zowazira, ndi zikho za golidi
woona, ndi ca mitsuko yace yagolidi, woyesedwa kulemera kwace
mtsuko uli wonse; ndi ca mitsuko yasiliva woyesedwa kulemera
kwace mtsuko uli wonse; 18ndi ca guwa la nsembe lofukizapo la
golidi woyengetsa woyesedwa kulemera kwace, ndi cifaniziro ca
gareta wa akerubi agolidi akufunyulula mapiko ao ndi kuphimba
likasa la cipangano la Yehova. 19Conseci, anati Davide,
anandidziwitsa ndi kucilemba kucokera kwa dzanja la Yehova;
ndizo nchito zonse za cifaniziro ici. 20Ndipo Davide anati kwa
Solomo mwana wace, Limbika, nulimbe mtima, nucicite; usaopa,
kapena kutenga nkhawa; pakuti Yehova Mulungu, ndiye Mulungu
wanga, ali nawe; sadzakusowa kapena kukutaya mpaka zitatha
nchito zonse za utumiki wa nyumba ya Yehova. 21Ndipo taona, pali
zigawo za ansembe ndi Alevi, za utumiki wonse wa nyumba ya
Mulungu; ndipo pamodzi nawe mu nchito iri yonse pali onse ofuna
eni ace aluso, acite za utumiki uli wonse; akuru omwe ndi anthu
onse adzacita monga umo udzanenamo.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Zopereka zaufulu zomangira Kacisi

1Mfumu Davide ananenanso kwa khamu lonse, Mulungu wasankha
mwana wanga Solomo yekha, ndiye mnyamata ndi wosakhwima;
ndipo nchitoyi ndi yaikuru, pakuti cinyumbaci siciri ca munthu,
koma ca Yehova Mulungu. 2Ndi mphamvu yanga yonse tsono
ndakonzeratu nyumba ya Mulungu wanga, golidi wa zija zagolidi
ndi siliva wa zija zasiliva, ndi mkuwa wa zija zamkuwa, citsulo ca
zija zacitsulo, ndi mtengo wa zija zamtengo, miyala yaberulo, ndi
miyala yoikika, miyala yokometsera, ndi ya mawanga mawanga,
ndi miyala ya mtengo wace ya mitundu mitundu ndi miyala
yansangalabwe yocuruka. 3Ndiponso popeza ndikondwera nayo
nyumba ya Mulungu wanga, cuma cangacanga ca golidi ndi siliva
ndiri naco ndicipereka ku nyumba ya Mulungu wanga, moenjezera
ndi zonse ndazikonzeratu nyumba yopatulikayo; 4ndico matalente
zikwi zitatu za golidi, golidi wa Ofiri; ndi matalente zikwi zisanu ndi
ziwiri a siliva woyengetsa, kumamatiza nazo makoma a
nyumbazi; 5golidi wa zija zagolidi, ndi siliva wa zija zasiliva, ndi za
nchito ziri zonse akuzipanga manja a amisiri. Ndani uyo afuna
mwini kudzipatulira kwa Yehova lero line? 6Pamenepo akuru a
nyumba za makolo, ndi akuru a mafuko a Israyeli, ndi akuru a zikwi
ndi a mazana pamodzi ndi iwo oyang'anira nchito ya mfumu,
anapereka mwaufulu, 7napereka ku utumiki wa nyumba ya
Mulungu golidi matalente zikwi zisanu, ndi madariki zikwi khumi;
ndi siliva matalente zikwi khumi, ndi mkuwa matalente zikwi khumi
mphambu zisanu ndi zitatu, ndi citsulo matalente zikwi zana
limodzi. 8Ndipo amene anali nayo miyala ya mtengo wace
anaipereka ku cuma ca nyumba ya Yehova, mwa dzanja la Yehieli
Mgerisoni. 9Ndipo anthu anakondwera popeza anapereka
mwaufulu; pakuti ndi mtima wangwiro anapereka mwaufulu kwa
Yehova; mfumu Davide yemwe anakondwera ndi cimwemwe
cacikuru.

Pemphero la Davide, ndi kumwalira kwace

10Motero Davide analemekeza Yehova pamaso pa khamu lonse,
nati Davide, Wolemekezedwa Inu, Yehova Mulungu wa Israyeli,
Atate wathu ku nthawi zomka muyaya. 11Ukulu, ndi mphamvu, ndi
ulemerero, ndi kulakika, ndi cifumu ndi zanu, Yehova; pakuti zonse
zam'mwamba ndi pa dziko lap ansi ndi zanu; ufumu ndi wanu,
Yehova; ndipo mwakwezeka mutu wa pa zonse. 12Zolemera ndi
ulemu zifuma kwanu, ndipo mucita ufumu pa zonse, ndi m'dzanja
mwanu muli mphamvu yaikuru; kukuza ndi kupatsa onse
mphamvu kuli m'dzanja lanu. 13Motero tsono, Mulungu wathu,
tikuyamikani ndi kulemekeza dzina lanu lokoma. 14Kama ndine
yani, ndi anthu anga ndiwo ayani, kuti tidzakhoza kupereka

mwaufulu motere? popeza zonsezi zifuma kwanu; takupatsani zofuma ku dzanja lanu. 15Pakuti ife ndife alendo pamaso panu, ndi ogonera, monga makolo athu onse; masiku athu a padziko akunga mthunzi, ndipo palibe kukhalitsa. 16Yehova Mulungu wathu, zounjikika izi zonse tazikonzeratu kukumangirani Inu nyumba ya dzina lanu loyera zifuma ku dzanja lanu, zonsezi ndi zanu. 17Ndidziwanso, Mulungu wanga, kuti muyesa mtima, nimukondwera nako kuongoka. Kama ine, ndi mtima wanga woongoka ndapereka zonsezi mwaufulu; ndipo tsopano ndaona mokondwera anthu anu okhala pompano, napereka kwa Inu mwaufulu. 18Yehova Mulungu wa Abrahamu, wa Isake, ndi wa Israyeli makolo athu, musungitse ici kosatha m'cilingaliro ca maganizo a mtima wa anthu anu, nimulunjikitse mitima yao kwanu, 19nimupatse Solomo mwana wanga mtima wangwiro kusunga malamulo anu, mboni zanu, ndi malemba anu, ndi kucita izi zonse, ndi kumanga cinyumbaci cimene ndakonzeratu mirimo yace, 20Ndipo Davide anati kwa khamu lonse, Mulemekeze tsono Yehova Mulungu wanu. Ndi khamu lonse linalemekeza Yehova Mulungu wa makolo ao, nawerama, nalambira Yehova, ndi mfumu. 21Ndipo anamphera Yehova nsembe, napereka nsembe zopsereza kwa Yehova m'mawa mwace mwa tsiku lija, ndizo ng'ombe cikwi cimodzi, nkhosa zamphongo cikwi cimodzi, ndi ana a nkhosa cikwi cimodzi, pamodzi ndi nsembe zao zothira, ndi nsembe zocuruka za Aisrayeli onse: 22nadya namwa pamaso pa Mulungu tsiku lomwelo ndi cimwemwe cacikuru. Ndipo analonga ufumu Solomo mwana wa Davide kaciwiri, namdzozera Yehova akhale kalonga, ndi Zadoki akhale wansembe. 23Momwemo Solomo anakhala pa mpando wacifumu wa Yehova, ndiye mfumu m'malo mwa Davide atate wace, nalemerera, nammvera iye Aisrayeli onse. 24Ndi akuru onse, ndi amuna amphamvu onse, ndi ana amuna onse omwe a mfumu Davide, anagonjeratu kwa Solomo mfumu. 25Ndipo Yehova anakuza Solomo kwakukuru pamaso pa Aisrayeli onse, nampatsa ulemerero wacifumu, wakuti, asanakhale iyeyu, panalibe mfumu ya Israyeli inali nao wotero. 26Momwemo Davide mwana wa Jese adakhala mfumu ya Aisrayeli onse. 27Ndipo nthawi yoti anakhala mfumu ya Israyeli ndiyo zaka makumi anai; zaka zisanu ndi ziwiri anakhala mfumu m'Hebroni, ndi zaka makumi atatu anakhala mfumu m'Yerusalemu. 28Nafa atakalamba bwino, wocuruka masiku, zolemera, ndi ulemerero; ndi Solomo mwana wace anakhala mfumu m'malo mwaceo 29Zocita mfumu Davide tsono, zoyamba ndi zotsiriza, taonani, zalembedwa m'buku la mau a Samueli mlauli, ndi m'buku la mau a Natani mneneri, ndi m'buku la mau a Gadi mlauli; 30pamodzi ndi za ufumu

wace wonse, ndi mphamvu yace, ndi za nthawizo zidampitira iye, ndi Israyeli, ndimaufumu onse a maiko.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Ezra

Ezara 1

Mulungu apangira Koresi alole Ayuda abwere kwao kukamanga Kacisi

1CAKA coyamba tsono ca Koresi mfumu ya ku Perisiya, kuti
akwaniridwe mau a Yehova m'kamwa mwa Yeremiya, Yehova
anautsa mzimu wa Koresi, kuti abukitse mau m'ufumu wace
wonse, nawalembenso, ndi kuti, 2Atero Koresi mfumu ya ku
Perisiya, Yehova Mulungu Wam'mwamba anandipatsa maufumu
onse a pa dziko lapansi, nandilangiza ndimmangire nyumba
m'Yerusalemu, ndiwo m'Yuda. 3Ali yense mwa inu a anthu ace
onse, Mulungu wace akhale naye, akwere kumka ku Yerusalemu,
ndiwo m'Yuda, nakaimange nyumba ya Yehova Mulungu wa
Israyeli; Iye ndiye Mulungu wokhala m'Yerusalemu. 4Ndipo ali
yense wotsala pamalo pali ponse agonerapo iye, anthu a kumalo
kwace amthandize ndi siliva, ndi golidi, ndi zoweta, ndi cuma,
pamodzi ndi nsembe yaufulu ya kwa nyumba ya Mulungu iri ku
Yerusalemu. 5Pamenepo ananyamuka akulu a nyumba za makolo a
Yuda ndi Benjamini, ndi ansembe, ndi Alevi, ndiwo onse amene
Mulungu adawautsira mzimu wao akwere kukamanga nyumba ya
Yehova iri ku Yerusalemu. 6Ndipo onse akuwazinga analimbitsa
manja ao ndi zipangizo za siliva, ndi golidi, ndi cuma, ndi zoweta,
ndi zinthu za mtengo wace, pamodzi ndi nsembe zaufulu.

Koresi abweza zipangizo za Kacisi

7Koresi mfumu anaturutsanso zipangizo za nyumba ya Yehova,
zimene Nebukadinezara adaziturutsa m'Yerusalemu, ndi kuziika
m'nyumba ya milungu yace; 8zomwezi Koresi mfumu ya ku Perisiya
anaziturutsa ndi dzanja la Miteridati wosunga cumayo,
naziwerengera Sezibazara kalonga wa Ayuda. 9Kuwerenga kwace
ndiko: mbizi zagolidi makumi atatu, mbizi zasiliva cikwi cimodzi,
mipeni makumi awiri mphambu isanu ndi inai; 10zikho zagolidi
makumi atatu, zikho zasiliva zina mazana anai ndi khumi,
zipangizo zina cikwi cimodzi. 11Zipangizo zonse zagolidi ndi zasiliva
ndizo zikwi zisanu ndi mazana anai. Izi zonse Sezibazara anakwera
nazo, pokwera andende aja kucokera ku Babulo kumka ku
Yerusalemu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Maina a Ayuda obwera ku Yerusalemu ndi Zerubabele

1Ana a deralo, amene anakwera kuturuka m'ndende mwa andende
aja Nebukadinezara mfumu ya Babulo adawatenga ndende kumka
nao ku Babulo, nabwerera kumka ku Yerusalemu ndi Yuda, yense
ku mudzi wace, ndi awa: 2ndiwo amene adadza ndi Zerubabele,
Yesuwa, Nehemiya, Seraya, Reelaya, Moredekai, Bilisani, Misipara,
Bigivai, Rehumu, Baana. Kuwerenga kwa amuna a anthu a Israyeli
ndiko: 3ana a Parosi, zikwi ziwiri ndi zana limodzi mphambu
makumi asanu ndi awiri kudza awiri. 4Ana a Sefatiya, mazana atatu
mphambu makumi asanu ndi awiri kudza awiri. 5Ana a Ara,
mazana asanu ndi awiri mphambu makumi asanu ndi awiri kudza
asanu. 6Ana a Pahati Moabu, a ana a Yesuwa ndi Yoabu, zikwi ziwiri
mphambu mazana asanu ndi atatu kudza khumi ndi awiri. 7Ana a
Elamu, cikwi cimodzi mphambu mazana awiri kudza makumi asanu
ndi anai. 8Ana a Zatu, mazana asanu ndi anai mphambu makumi
anai kudza asanu. 9Ana a Zakai, mazana asanu ndi awiri mphambu
makumi asanu ndi limodzi. 10Ana a Bani, mazana asanu ndi limodzi
mphambu makumi anai kudza awiri. 11Ana a Bebai, mazana asanu
ndi limodzi mphambu makumi awiri kudza awiri. 12Ana a Asigadi,
cikwi cimodzi mphambu mazana awiri kudza makumi awiri ndi
awiri. 13Ana a Adonikamu, mazana asanu ndi limodzi mphambu
makumi asanu ndi limodzi kudza asanu ndi mmodzi. 14Ana a
Bigivai, zikwi ziwiri mphambu makumi asanu kudza asanu ndi
mmodzi. 15Ana a Adini, mazana anai mphambu makumi asanu
kudza anai. 16Ana a Ateri, a Hezekiya, makumi asanu ndi anai
mphambu asanu ndi atatu. 17Ana a Bezai, mazana atatu mphambu
makumi awiri kudza atatu. 18Ana a Yora, zana limodzi mphambu
khumi ndi awiri. 19Ana a Hasumu, mazana awiri mphambu makumi
awiri kudza atatu. 20Ana a Gibara, makumi asanu ndi anai
mphambu asanu. 21Ana a Betelehemu zana limodzi mphambu
makumi awiri kudza atatu. 22Anthu a ku Netofa, makumi asanu
mphambu asanu ndi mmodzi. 23Anthu a ku Anatoti, zana limodzi
mphambu makumi awiri kudza asanu ndi atatu. 24Ana a Azimaveti,
makumi anai mphambu awiri. 25Ana a Kiriyati Arimu, Kefira, ndi
Beeroti, mazana asanu ndi awiri mphambu makumi anai kudza
atatu. 26Ana a Rama ndi Gaba, mazana asanu ndi limodzi
mphambu makumi awiri kudza mmodzi. 27Anthu a Mikimasi, zana
limodzi mphambu makumi awiri kudza awiri. 28Anthu a ku Beteli
ndi Ai, mazana awiri mphambu makumi awiri kudza atatu. 29Ana a
Nebo, makumi asanu mphambu awiri. 30Ana a Magabisi, zana
limodzi mphambu makumi asanu kudza asanu ndi mmodzi. 31Ana
a Elamu wina, cikwi cimodzi mphambu mazana awiri kudza
makumi asanu ndi anai. 32Ana a Harimu, mazana atatu mphambu

makumi awiri. 33Ana a Lodi, Hadidi, ndi Ono, mazana asanu ndi awiri mphambu makumi awiri kudza asanu. 34Ana a Yeriko, mazana atatu mphambu makumi anai kudza asanu. 35Ana a Senai, zikwi zitatu mphambu mazana asanu ndi limodzi kudza makumi atatu. 36Ansembe: ana a Yedaya, a nyumba ya Yesuwa, mazana asanu ndi anai mphambu makumi asanu ndi awiri kudza atatu. 37Ana a lmneri, cikwi cimodzi mphambu makumi asanu kudza awiri. 38Ana a Pasuru, cikwi cimodzi mphambu mazana awiri kudza makumi anai ndi asanu ndi awiri. 39Ana a Harimu, cikwi cimodzi mphambu khumi limodzi kudza asanu ndi awiri. 40Alevi: ana a Yesuwa, ndi Kadimiyeli, ndiwo a ana a Hodariya, makumi asanu ndi awiri mphambu anai. 41Oyimba: ana a Asafu, zana limodzi mphambu makumi awiri kudza asanu ndi atatu. 42Ana a odikira: ana a Sabumu, ana a Ateri, ana a Talimoni, ana a Akubu, ana a Hatita, ana a Sobai, onse pamodzi ndiwo zana limodzi mphambu makumi atatu kudza asanu ndi anai. 43Anetini: ana a Ziha, ana a Hasufa, ana a Tabaoti, 44ana a Kerosi, ana a Siaha, ana a Padoni, 45ana a Lebano, ana a Hagaba, ana a Akubu, 46ana a Hagabu, ana a Salimai, ana a Hanani, 47ana a Gideli, ana a Gahari, ana a Reaya, 48ana a Rezini, ana a Nekoda, ana a Gazamu, 49ana a Uza, ana a Paseya, ana a Besai, 50ana a Asina, ana a Mehunimu, ana a Nefusimu, 51ana a Bakabuku, ana a Hakufa, ana a Haruri, 52ana a Baziluti, ana a Mehida, ana a Harisa, 53ana a Barikosi, ana a Siseri, ana a Tama, 54ana a Neziya, ana a Hatifa. 55Ana a akapolo a Solomo: ana a Sotai, ana a Sofereti, ana a Peruda, 56ana a Yaala, ana a Darikoni, ana a Gideli, 57ana a Sefatiya, ana a Hatili, ana a Pokereti wa Zebaimu, ana a Ami. 58Anetini onse, ndi ana a akapolo a Solomo, ndiwo mazana atatu mphambu makumi asanu ndi anai kudza awiri. 59Ndipo okwera kucokera ku Telemela, Teleharisa, Kerubi, Adana, Imeri, ndi awa, koma sanakhoza kuchula nyumba za makolo ao ndi mbumba zao ngati ali Aisrayeli: 60ana a Delaya, ana a Tobiya, ana a Nekoda, mazana asanu ndi limodzi mphambu makumi asanu kudza awiri. 61Ndi ana a ansembe: ana a Habaya, ana a Kozi, ana a Barizilai, amene anadzitengera mkazi wa ana akazi a Barizilai Mgileadi, nachedwa dzina lao. 62Awa anafunafuna maina ao m'buku la iwo owerengedwa mwa cibadwidwe cao, koma osawapeza; potero anacotsedwa ku nchito ya nsembe monga odetsedwa. 63Ndipo kazembe anawauza kuti asadyeko zopatulikitsa, mpaka adzabuka wansembe wokhala ndi Urimu ndi Tumimu. 64Msonkhano wonse pamodzi ndiwo wa zikwi makumi anai ndi awiri mphambu mazana atatu kudza makumi asanu ndi limodzi, 65osawerenga akapolo ao amuna ndi akazi, ndiwo zikwi zisanu ndi ziwiri mphambu mazana atatu ndi makumi atatu kudza

asanu ndi awiri; ndipo anakhala nao amuna ndi akazi oyimbira
mazana awiri. 66Akavalo ao ndiwo mazana asanu ndi awiri
mphambu makumi atatu kudza asanu ndi mmodzi; nyuru zao
mazana awiri mphambu makumi anai kudza zisanu; 67ngamira zao
mazana anai mphambu makumi atatu kudza asanu; aburu zikwi
zisanu ndi cimodzi mphambu mazana asanu ndi awiri kudza
makumi awiri. 68Ndipo akulu ena a nyumba za makolo, pofika ku
nyumba ya Yehova iri ku Yerusalemu, anapereka caufulu kwa
nyumba ya Mulungu cakulimika pakuzika pace. 69Monga momwe
anakhoza anapereka ku cuma ca nchitoyi madariki agolidi: zikwi
zisanu ndi cimodzi, miyeso ya siliva zikwi zisanu, ndi maraya a
ansembe zana limodzi. 70Ndipo ansembe, ndi Alevi, ndi anthu ena,
ndi oyimbira, ndi odikira, ndi Anetini, anakhala m'midzi mwao, ndi
Aisrayeli onse m'midzi mwao.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Ezara 3

Limangidwa guwa la nsembe

1Utakhala tsono mwezi wacisanu ndi ciwiri, ana a Israyeli ali
m'midzimo, anthuwo anasonkhana ngati munthu mmodzi ku
Yerusalemu. 2Nanyamuka Yesuwa mwana wa Yozadaki, ndi abale
ace ansembe, ndi Zerubabele mwana wa Sealitiyeli, ndi abale ace,
namanga guwa la nsembe la Mulungu wa Israyeli, kuperekapo
nsembe zopsereza, monga mulembedwa m'cilamulo ca Mose
munthu wa Mulungu. 3Ndipo anakhazika guwa la nsembe patsinde
pace cifukwa ca kuopa iwo anthu a m'maikomo; nakwezera Yehova
nsembe zopsereza pamenepo, nsembe zopsereza zam'mawa ndi
zamadzulo. 4Nacita madyerero a misasa monga kwalembedwa,
napereka nsembe yopsereza tsiku ndi tsiku mawerengedwe ace,
monga mwa lamulo lace la tsiku lace pa tsiku lace; 5atatero
anaperekanso nsembe yopsereza yosalekeza, ndi za pokhala
mwezi, ndi za nyengo zoikika zonse za Yehova zopatulika, ndi za
munthu yense wopereka nsembe yaufulu kwa Yehova
mwaufulu. 6Ciyambire tsiku loyamba la mwezi wacisanu ndi ciwiri
anapereka nsembe zopsereza kwa Yehova; koma sanamange
maziko a Kacisi wa Yehova. 7Anaperekanso ndarama kwa amisiri a
miyala, ndi a mitengo; ndi cakudya, ndi cakumwa, ndi mafuta, kwa
a ku Sidoni, ndi a ku Turo, kuti atenge mikungudza ku Lebano,
kufika nayo ku nyanja ku Yopa, monga adawalola Koresi mfumu ya
Babulo.

Aika maziko a Kacisi

8Caka caciwiri tsono cakufika iwo ku nyumba ya Mulungu ku
Yerusalemu, mwezi waciwiri, Zerubabele mwana wa Sealitiyeli, ndi
Yesuwa mwana wa Yozadaki, ndi abale ao otsala, ansembe ndi
Alevi ndi onse ocokera kundende kudza ku Yerusalemu, anayamba,
naika Alevi a zaka makumi awiri ndi mphambu, ayang'anire nchito
ya nyumba ya Yehova. 9Pamenepo anaimirira pamodzi Yesuwa ndi
ana ace ndi abale ace, Kadimiyeli ndi ana ace, ana a Yuda,
kuyang'anira ogwira nchito m'nyumba ya Yehova, ana a Henadadi
ndi ana ao ndi abale ao Alevi. 10Ndipo pomanga maziko a Kacisi wa
Yehova, amisiriwo anaimiritsa ansembe obvala zobvala zao ndi
mphalasa, ndi Alevi ana a Asafu ndi nsanje, kuti alemekeze
Yehova, monga umo anaikiratu Davide mfumu ya Israyeli. 11Ndipo
anathirirana mang'ombe, kulemekeza ndi kuyamika Yehova, ndi
kuti, Pakuti ndiye wabwino, pakuti cifundo cace ncosalekeza pa
Israyeli. Napfuula anthu onse ndi cipfuu cacikuru, pomlemekeza
Yehova; popeza adamanga maziko a nyumba ya Yehova. 12Koma
ansembe ambiri, ndi Alevi, ndi akuru a nyumba za makolo,
okalamba amene adaona nyumba yoyamba ija, pomanga maziko a
nyumba iyi pamaso pao, analira ndi mau akuru; koma ambiri

anapfuulitsa mokondwera. 13Potero anthu sanazindikira phokoso la kupfuula mokondwera kulisiyanitsa ndi phokoso la kulira kwa anthu; pakuti anthu anapfuulitsa kwakukuru, ndi phokoso lace lidamveka kutari.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Ezara 4

Asamariya aneneza Ayuda omanga Kacisi kwa Ahaswero

1Atamva tsono a adani Yuda ndi Benjamini kuti ana aja a ndende
analikumangira Yehova Mulungu wa Israyeli Kacisi, 2anayandikira kwa
Zerubabele, ndi kwa akulu a nyumba za makolo, nanena nao, Timange
pamodzi nanu; pakuti timfuna Mulungu wanu monga inu, ndipo timamphera
nsembe ciyambire masiku a Ezaradoni mfumu ya Asuri, amene anatikweretsa
kuno. 3Koma Zerubabele, ndi Yesuwa, ndi akuru otsala a nyumba za makolo a
Israyeli, anati kwa iwo, Sikuyenera ndi inu ndi ife kumangira Mulungu wathu
nyumba, koma ife tokha pamodzi tidzamangira Yehova Mulungu wa Israyeli,
monga mfumu Koresi mfumu ya Perisiya watilamulira. 4Pamenepo anthu a
m'dziko anafoketsa manja a anthu Ayuda, nawabvuta pomanga, 5nalembera
opangira atsutsane nao, nafafanize uphungu wao, masiku onse a Koresi
mfumu ya Perisiya, mpaka ufumu wa Dariyo mfumu ya Perisiya. 6Ndipo
pokhala mfumu Ahaswero, poyambira ufumu wace, analembera cowaneneza
okhala m'Yuda ndi m'Yerusalemu.
7Ndipo masiku a Aritasasta Bisilamu, Mitiredati, Tabeeli, ndi anzao otsala,
analembera kwa Aritasasta mfumu ya Perisiya; ndi cilembedwe cace ca
kalatayo anamlemba m'Ciaramu, namsanduliza m'Ciaramu. 8Rehumu ciwinda
ca malamulo, ndi Simsai mlembi, analemba kalata kwa mfumu Aritasasta,
wakutsutsana naye Yerusalemu motere: 9nalembera Rehumu ciwinda ca
malamulo, ndi Simsai mlembi, ndi anzace otsala; Adinai, ndi Afarisatikai,
Ataripilai, Afarisai, Arekavai, Ababulo, Asusanekai, Adehai, Aelimai, 10ndi
amitundu otsala amene, Osinapera wamkuru ndi womveka adawatenga
mikoli, nawakhalitsa m'mudzi wa Samariya, ndi m'dziko lotsala tsidya lino la
mtsinje wa Firate, pa nthawi yakuti. 11Zolembedwa m'kalatayo anamtumiza
kwa Aritasasta mfumu ndizo: Akapolo anu, anthu a tsidya lino la mtsinjewo,
ndi pa nthawi yakuti. 12Adziwe mfumu kuti, Ayuda adakwerawo ocokera
kwanu atifikira ife ku Yerusalemu, alikumanga mudzi uja wopanduka ndi
woipa, alikutsiriza malinga ace, nalumikiza maziko ace. 13Adziwe tsono
mfumu, kuti akamanga mudzi uwu ndi kutsiriza malinga ace, sadzapereka
msonkho, kapena thangata, kapena msonkho wa m'njira; ndipo potsiriza pace
kudzasowetsa mafumu. 14Popeza tsono timadya mcere wa m'nyumba ya
mfumu, sitiyenera kungopenyerera mpepulo wa pa mfumu; cifukwa cace
tatumiza ndi kudziwitsa mfumu, 15kuti afunefune m'buku la cikumbutso la
makolo anu; momwemo mudzapeza m'buku la cikumbutso, ndi kudziwa kuti
mudzi uwu ndi mudzi wopanduka, ndi wosowetsa mafumu, ndi maiko; ndi kuti
amadziyendera m'menemo kuyambira kale lomwe; ndico cifukwa cakuti
anapasula mudzi uwu. 16Tirikudziwitsa mfumu kuti ukamangidwa mudziwu,
nakatsirizidwa malinga ace, simudzakhala nalo gawo tsidya lino la mtsinjewo.

Mfumu iwaletsa asamange Kacisi

17Mfumu nibweza mau kwa Rehumu ciwinda ca malamulo, ndi kwa Simsai
mlembi, ndi kwa anzao otsala okhala m'Samariya, ndi otsala tsidya lino la
mtsinjewo, Mtendere, ndi nthawi yakuti. 18Kalatayo mwatitumizira
anandiwerengera momveka. 19Ndipo ndinalamulira anthu, nafunafuna,
napeza kuti mudzi uwu unaukira mafumu kuyambira kale lomwe ndi kuti
akacitamo mpanduko ndi kudziyendera. 20Panalinso mafumu amphamvu
m'Yerusalemu amene anacita ufumu tsidya lija lonse la mtsinje, ndipo anthu
anawapatsa msonkho, thangata, ndi msonkho wa m'njira. 21Mulamulire tsono
kuti anthu awa aleke, ndi kuti asamange mudzi uwu, mpaka ndidzalamulira
ndine. 22Cenjerani mungadodomepo, cidzakuliranji cisauko ca kusowetsa
mafumu? 23Pamenepo atawerenga malemba a kalata wa mfumu kwa

Rehumu, ndi Simsai mlembi, ndi anzao, anafulumira kupita ku Yerusalemu kwa Ayuda, nawaletsa ndi dzanja lamphamvu. 24Momwemo inalekeka nchito ya nyumba ya Mulungu yokhala ku Yerusalemu; nilekeka mpaka caka caciwiri ca ufumu wa Dariyo mfumu ya Perisiya.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Ezara 5

Zerubabele ndi Yesuwa apitirira kumanga Kacisi

1Ndipo aneneri, Hagai mneneriyo, ndi Zekariya mwana wa Ido, ananenera kwa Ayuda okhala m'Yuda ndi m'Yerusalemu; m'dzina la Mulungu wa Israyeli ananenera kwa iwo. 2Pamenepo Zerubabele mwana wa Sealitiyeli, ndi Yesuwa mwana wa Yozadaki, ananyamuka, nayamba kumanga nyumba ya Mulungu iri ku Yerusalemu, anali pamodzi nao aneneri a Mulungu akuwathandiza. 3Nthawi yomweyi anawadzera Tatinai kazembe tsidya lino la mtsinjewo, ndi Setara Bozinai, ndi anzao, nanena nao motere, Anakulamulirani inu ndani kumanga nyumba iyi, ndi kutsiriza khoma ili? 4Nanena naonso motere, Maina ao a anthu omanga cimangidwe ici ndiwo ayani? 5Koma diso la Mulungu wao linali pa akuru a Ayuda, ndipo sanawaletsa mpaka mlandu unamdzera Dariyo, nabweza mau a mlanduwo m'kalata.

Tatinai awaneneza kwa Dariyo

6Zolembedwa m'kalata amene Tatinai kazembe wa tsidya lino la mtsinjewo, ndi Setara Bozenai, ndi anzace Afarisikai, okhala tsidya lino la mtsinje, anatumiza kwa Dariyo mfumu, 7anatumiza kalata kwa iyeyo m'menemo munalembedwa motere, Kwa Dariyo mfumu, mtendere wonse. 8Adziwe mfumu kuti ife tinamuka ku dziko la Yuda, ku nyumba ya Mulungu wamkuru, yomangidwa ndi miyala yaikuru, niikidwa mitengo pamakoma, nicitika mofulumira nchitoyi, nikula m'dzanja mwao. 9Pamenepo tinafunsa akulu aja ndi kutere nao, Anakulamulirani ndani kumanga nyumba iyi, ndi kutsiriza khoma ili? 10Tinawafunsanso maina ao, kukudziwitsani, kuti tilembere maina a anthu akuwatsogolera. 11Natiyankha mau motere, ndi kuti, Ife ndife akapolo a Mulungu wa Kumwamba ndi dziko lapansi, tirikumanga nyumba imene idamangika zapita zaka zambiri; inaimanga ndi kuitsiriza mfumu yaikuru ya Israyeli. 12Koma makolo athuwo atautsa mkwiyo wa Mulungu wa Kumwamba, Iye anawapereka m'dzanja la Nebukadinezara mfumu ya ku Babulo Mkasidi, amene anaononga nyumba yino, natenga anthu ndende kumka nao ku Babulo. 13Koma caka coyamba ca Koresi mfumu ya Babulo, Koresi mfumuyo analamulira kuti azimanga nyumba iyi ya Mulungu. 14Ndiponso zipangizo za golidi ndi siliva za nyumba ya Mulungu, anaziturutsa Nebukadinezara m'Kacisi anali ku Yerusalemu, ndi kubwera nazo ku kacisi wa ku Babulo, izizo Koresi mfumu anaziturutsa m'kacisi wa ku Babulo, nazipereka kwa munthu dzina lace Sezibazara, amene anamuika akhale kazembe; 15nati naye, Tenga zipangizo izi, kaziike m'Kacisi ali m'Yerusalemu, nimangidwe nyumba ya Mulungu pambuto pace. 16Pamenepo anadza Sezibazara yemweyo namanga maziko a nyumba ya Mulungu iri m'Yerusalemu; ndipo kuyambira

pomwepo kufikira tsopano irimkumangidwa, koma
siinatsirizike. 17Ndipo tsono cikakomera mfumu, munthu asanthule
m'nyumba ya cuma ca mfumu iri komwe ku Babulo, ngati
nkuterodi, kuti Koresi mfumu analamulira kuti azimanga nyumba
iyi ya Mulungu ku Yerusalemu; ndipo mfumu ititumizire mau
omkomera pa cinthuci.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Ezara 6

Dariyo anenetsa kuti Kacisi amangidwe

1Pamenepo analamulira Dariyo mfumu, ndipo anthu anafunafuna
m'nyumba ya mabuku mosungira cuma m'Babulo. 2Napeza ku
Akimeta m'nyumba ya mfumu m'dera la Mediya, mpukutu, ndi
m'menemo munalembedwa motere, cikhale cikumbutso: 3Caka
coyamba ca Koresi mfumu, analamulira Koresi mfumuyo, Kunena
za nyumba ya Mulungu ku Yerusalemu, imangidwe nyumbayi
pamalo pophera nsembe, namangidwe kolimba maziko ace,
msinkhu wace mikono makumi asanu ndi limodzi, kupingasa kwace
mikono makumi asanu ndi limodzi; 4ndi mipambo itatu ya miyala
yaikuru, ndi mpambo wa mitengo yatsopano; nalipidwe ndarama
zocokera ku nyumba ya mfumu. 5Ndi zipangizo za golidi ndi siliva
za nyumba ya Mulungu, zimene anaziturutsa Nebukadinezara
m'Kacisi ali ku Yerusalemu, nazitenga kumka nazo ku Babulo,
azibwezere, nabwere nazo ku Kacisi ali ku Yerusalemu, ciri conse
ku malo ace; naziike m'nyumba ya Mulungu. 6Tsono iwe, Tatinai,
kazembe wa tsidya lija la mtsinjewo, Setara Bozenai, ndi anzanu
Afarisikai, okhala tsidya lija la mtsinje, muzikhala kutali; 7lekani
nchito iyi ya Mulungu, osaibvuta; kazembe wa Ayuda ndi akulu a
Ayuda amange nyumba iyi ya Mulungu pambuto
pace. 8Ndilamuliranso za ici muzicitira akuru awa a Ayuda, kuti
amange nyumba iyi ya Mulungu, ndiko kuti mutengeko cuma ca
mfumu, ndico msonkho wa tsidya la mtsinje, nimupereke zolipira
kwa anthu awa msanga, angawacedwetse. 9Ndipo zosowa zao, ana
a ng'ombe, ndi nkhosa zamphongo, ndi ana a nkhosa, zikhale
nsembe zopsereza za Mulungu wa Kumwamba; tirigu, mcere,
vinyo, mafuta, monga umo adzanena ansembe ali ku Yerusalemu,
ziperekedwe kwa iwo tsiku ndi tsiku, zisasoweke; 10kuti apereke
nsembe zonunkhira bwino kwa Mulungu wa Kumwamba,
napempherere moyo wa mfumu ndi wa ana ace. 11Ndalamuliranso
kuti ali yense adzasintha mau awa, usololedwe mtanda kunyumba
kwace, namkweze, nampacike pomwepo; niyesedwe dzala nyumba
yace cifukwa ca ici; 12ndipo Mulungu wokhalitsa dzina lace
komweko agwetse mafwnu onse ndi mitundu yonse ya anthu,
akuturutsa dzanja lao kusintha mau awa, kuononga nyumba ya
Mulungu iri ku Yerusalemu. Ine Dariyo ndalamulira, cicitike
msanga.
13Pamenepo Tatinai kazembe wa tsidya lino la mtsinjewo, Setara
Bozenai, ndi anzao, popeza mfumu Dariyo adatumiza mau, anacita
momwemo cofulumira. 14Ndipo akulu a Ayuda anamanga opanda
cosoweka, mwa kunenera kwa mneneri Hagai, ndi Zekariya mwana
wa Ido. Naimanga, naitsiriza, monga mwa lamulo la Mulungu wa
Israyeli, ndi monga mwa lamulo la Koresi, ndi Dariyo, ndi Aritasasta

mfumu ya Perisiya, 15Nitsirizidwa nyumba iyi tsiku lacitatu la
mwezi wa Adara, ndico caka cacisanu ndi cimodzi ca ufumu wa
Dariyo mfumu.

Apereka Kacisi nacita Paskha

16Ndipo ana a Israyeli, ansembe ndi Alevi, ndi ana otsala a ndende,
anapereka nyumba iyi ya Mulungu mokondwera. 17Ndipo
popatulira nyumba iyi ya Mulungu anapereka ng'ombe zana
limodzi, nkhosa zamphongo mazana awiri, ana a nkhosa mazana
anai, ndi za nsembe yazolakwa ya Aisrayeli onse atonde khumi ndi
awiri, monga mwa kuwerenga kwace kwa mapfuko a
Israyeli. 18Naika ansembe m'magawo mwao, ndi Alevi
m'magawidwe mwao, atumikire Mulungu wokhala ku Yerusalemu,
monga mulembedwa m'buku la Mose.
19Ndipo ana a ndende anacita Paskha tsiku lakhumi ndi cinai la
mwezi woyamba. 20Pakuti ansembe ndi Alevi anadziyeretsa
pamodzi, anayera onsewo, naphera Paskha cifukwa ca ana onse a
ndende, ndi abale ao ansembe, ndi iwo okha. 21Ndipo ana a
Israyeli obwera kundende, ndi yense wakudzipatulira kucokera
conyansa ca amitundu, kutsata iwowa, kufuna Yehova Mulungu wa
Israyeli, anadza, 22nasunga madyerero a mkate wopanda cotupitsa
masiku asanu ndi awiri ndi cimwemwe; pakuti Yehova
adawakondweretsa, nawatembenuzira mtima wa mfumu ya Asuri,
kulimbitsa manja ao mu nchito ya nyumba ya Mulungu, Mulungu
wa Israyeli.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Ezara 7

Aritasasta atumiza Ezara ku Yerusalemu akonzenso cipembedzo ca Yehova

1Zitatha izi tsono, pokhala mfumu Aritasasta mfumu ya Perisiya,
anadza Ezara mwana wa Seraya, mwana wa Azariya, mwana wa
Hilikiya, 2mwana wa Salumu, mwana wa Zadoki, mwana wa
Ahitubu, 3mwana wa Amariya, mwana wa Azariya, mwana wa
Meraioti, 4mwana wa Zerahiya, mwana wa Uzi, mwana wa
Buki, 5mwana wa Abisuwa mwana wa Pinehasi, mwana wa
Eleazara, mwana wa Aroni wansembe wamkuru. 6Ezara amene
anakwera kucokera ku Babulo, ndiye mlembi waluntha m'cilamulo
ca Mose, cimene Yehova Mulungu wa Israyeli adacipereka; ndipo
mfumu inampatsa copempha iye conse, monga linamkhalira
dzanja la Yehova Mulungu wace. 7Nakweranso kumka ku
Yerusalemu ena a ana a Israyeli, ndi ansembe, ndi Alevi, ndi
oyimbira, ndi odikira, ndi Anetini, caka cacisanu ndi ciwiri ca
Aritasasta mfumu. 8Ndipo iye anafika ku Yerusalemu mwezi
wacisanu, ndico caka cacisanu ndi ciwiri ca mfumu. 9Pakuti tsiku
loyamba la mwezi woyamba, ndilo ciyambi ca ulendo wokwera
kucokera ku Babulo, ndi tsiku lacimodzi la mwezi wacisanu anafika
ku Yerusalemu, monga linamkhalira dzanja lokoma la Mulungu
wace. 10Pakuti Ezara adaikiratu mtima wace kucifuna cilamulo ca
Yehova, ndi kucicita, ndi kuphunzitsa m'Israyeli malemba ndi
maweruzo.
11Malemba a kalatayo mfumu Aritasasta anampatsa Ezara
wansembe mlembi, ndiye mlembi wa mau a malamulo a Yehova,
ndi malemba ace kwa Israyeli, ndi awa: 12Aritasasta mfumu ya
mafumu kwa Ezara wansembe, mlembi wa lamulo la Mulungu wa
Kumwamba, mtendere weni weni, ndi pa nthawi
yakuti. 13Ndilamulira kuti onse a ana a Israyeli, ndi ansembe ao,
ndi Alevi, m'ufumu wanga, ofuna eni ace kumuka ku Yerusalemu,
apite nawe. 14Popeza utumidwa wocokera pamaso pa mfumu ndi
aphungu ace asanu ndi awiri, kufunsira za Yuda ndi Yerusalemu
monga mwa lamulo la Mulungu wako liri m'dzanja lako, 15ndi
kumuka nazo siliva ndi golidi, zimene mfumu ndi aphungu ace,
anapereka mwaufulu kwa Mulungu wa Israyeli, mokhala mwace
muli m'Yerusalemu, 16pamodzi ndi siliva ndi golidi ziri zonse
ukazipeza m'dziko lonse la ku Babulo, pamodzi ndi copereka
caufulu ca anthu, ndi ca ansembe, akuperekera mwaufulu nyumba
ya Mulungu wao iri ku Yerusalemu; 17m'mwemo uzifulumira kugula
ndi ndalama iyi ng'ombe, nkhosa zamphongo, ana a nkhosa,
pamodzi ndi nsembe zao zaufa, ndi nsembe zao zothira; ndi
kuzipereka pa guwa la nsembe la nyumba ya Mulungu wanu
yokhala ku Yerusalemu. 18Ndipo ciri conse cidzakomera iwe ndi

abale ako kucita nazo siliva ndi golidi zotsala, ici mucite monga
mwa cifuniro ca Mulungu wanu. 19Ndipo zipangizozo akupatsa za
utumiki wa nyumba ya Mulungu wako, uzipereka pamaso pa
Mulungu wa ku Yerusalemu. 20Ndi zina zotsala zakusowa nyumba
ya Mulungu wako, zikayenera uzipereke, uzipereke zocokera ku
nyumba ya cuma ca mfumu. 21Ndipo ine Aritasasta, mfumu ine,
ndilamulira osunga cuma onse okhala tsidya lija la mtsinjewo, kuti
ciri conse akupemphani Ezara wansembe, mlembi wa lamulo la
Mulungu wa Kumwamba, cicitike mofulumira; 22mpaka matalente a
siliva zana limodzi, ndi miyeso ya tirigu zana limodzi, ndi miyeso
ya vinyo zana limodzi, ndi miyeso ya mafuta zana limodzi, ndi
mcere wosauwerenga. 23Ciri conse Mulungu wa Kumwamba
acilamulire cicitikire mwacangu nyumba ya Mulungu wa
Kumwamba; pakuti padzakhaliranji mkwiyo pa ufumu wa mfumu
ndi ana ace? 24Tikudziwitsaninso kuti sikudzaloledwa kusonkhetsa
ali yense wa ansembe, ndi Alevi, oyimbira, odikira, Anetini, kapena
anchito a nyumba iyi ya Mulungu msonkho, thangata, kapena
msonkho wa panjira. 25Ndipo iwe Ezara monga mwa nzeru za
Mulungu wako iri m'dzanja lako, uike nduna, ndi oweruza mirandu,
aweruze anthu onse ali tsidya lija la mtsinje, onse akudziwa
malamulo a Mulungu wako; ndi wosawadziwayo
umphunzitse. 26Ndipo ali yense wosacita lamulo la Mulungu wako,
ndi lamulo la mfumu, mlandu umtsutse msanga, ngakhale
kumupha, kapena kumpitikitsa m'dziko, kapena kumlanda cuma
cace, kapena kummanga m'kaidi.
27Wodala Yehova Mulungu wa makolo athu, amene anaika cinthu
cotere mu mtima wa mfumu, kukometsera nyumba ya Yehova iri
ku Yerusalemu, 28nandifikitsira cifundo pamaso pa mfumu, ndi
aphungu ace, ndi pamaso pa akalonga amphamvu onse a mfumu.
Motero ndinalimbika mtima, monga umo dzanja la Yehova Mulungu
wanga linakhala pa ine; ndipo ndinasonkhanitsa mwa Israyeli
anthu omveka akwere nane limodzi.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Ezara 8

Maina a opita ndi Ezara. Ulendo wao mpaka Yerusalemu

1Ndipo akuru a nyumba za makolo ndi awa, ndi cibadwidwe ca iwo
okwera nane limodzi kucokera ku Babulo, pokhala mfumu
Aritasasta, ndi ici: 2wa ana a Pinehasi, Gerisomu; wa ana a
Itamara, Danieli; wa ana a Davide, Hatusi. 3Wa ana a Sekaniya, wa
ana a Parosi, Zekariya; ndi pamodzi naye, powawerenga monga
mwa cibadwidwe cao, amuna zana limodzi mphambu makumi
asanu. 4Wa ana a Pahati Moabu, Elihoenai mwana wa Zerahiya; ndi
pamodzi naye amuna mazana awiri. 5Wa ana a Sekaniya, mwana
wa Yahazieli; ndi pamodzi naye amuna mazana atatu. 6Ndi wa ana
a Adini, Ebedi mwana wa Yonatani; ndi pamodzi naye amuna
makumi asanu. 7Ndi wa ana a Elamu, Yesaya mwana wa Ataliya;
ndi pamodzi naye amuna makumi asanu ndi awiri. 8Ndi wa ana a
Sefatiya, Zebadiya mwana wa Mikaeli; ndi pamodzi naye amuna
makumi asanu ndi atatu. 9Wa ana a Yoabu, Obadiya mwana wa
Yehieli; ndi pamodzi naye amuna mazana awiri mphambu khumi
kudza asanu ndi atatu. 10Ndi wa ana a Selomiti, mwana wa
Yosifiya; ndi pamodzi naye amuna zana limodzi mphambu makumi
asanu ndi limodzi. 11Ndi wa ana a Bebai, Zekariya mwana wa
Bebai; ndi pamodzi naye amuna makumi awiri mphambu asanu ndi
atatu. 12Ndi wa ana a Azigadi, Yohanana mwana wa Hakatana; ndi
pamodzi naye amuna zana limodzi mphambu khumi limodzi. 13Ndi
a ana otsiriza a Adonikmnu, maina ao ndiwo Elifeleti, Yeueli, ndi
Semaya; ndi pamodzi nao amuna makumi asanu ndi limodzi. 14Ndi
wa ana a Bigivai, Utai ndi Zabudi, ndi pamodzi nao amuna makumi
asanu ndi awiri.
15Ndipo ndinawasonkhanitsa ku mtsinje wopita ku Ahava, ndi
komweko tinakhala m'misasa masiku atatu; ndipo ndinapenyerera
anthu ndi ansembe, koma sindinapezapo wa ana a
Levi. 16Pamenepo ndinatumiza munthu kuitana Eliezere, Ariyeli,
Semaya, ndi Elimatana, ndi Natani, ndi Zekariya, ndi Mesulamu,
ndiwo akuru; ndi Yoyaribi ndi Elinatani, ndiwo aphunzitsi. 17Ndipo
ndinawatumiza kwa Ido mkuru, ku malo dzina lace Kasifiya;
ndinalooganso m'kamwa mwao mau akunena kwa Ido, ndi kwa
abale ace Anetini, pa malo paja Kasifiya, kuti azibwera nao kwa ife
otumikira za nyumba ya Mulungu wathu. 18Ndipo monga
munatikhalira dzanja lokoma la Mulungu wathu, anatitengera
munthu wanzeru wa ana a Mali, mwana wa Levi, mwana wa
Israyeli; ndi Serebiya, pamodzi ndi ana ace ndi abale ace khumi
mphambu asanu ndi atatu; 19ndi Hasabiya, ndi pamodzi naye
Yesaya wa ana a Merari, abale ace ndi ana ao makumi awiri; 20ndi
a Anetini, amene Davide ndi akalonga adapereka atumikire Alevi,
Anetini mazana awiri mphambu makumi awiri, onsewo ochulidwa

maina. 21Pamenepo ndinalalikira cosala komweko ku mtsinje wa
Ahava, kuti tidzicepetse pamaso pa Mulungu wathu, kumfunsa
ationetsere njira yolunjika ya kwa ife, ndi ang'ono athu, ndi cuma
cathu conse. 22Pakuti ndinacita manyazi kupempha kwa mfumu
gulu la asilikari, ndi apakavalo, kutithandiza pa adani panjira;
popeza tidalankhula ndi mfumu kuti, Dzanja la Mulungu wathu
likhalira mokoma onse akumfuna; koma mphamvu yace ndi
mkwiyo wace zitsutsana nao onse akumsiya. 23Momwemo tinasala
ndi kupempha ici kwa Mulungu wathu; natibvomereza
Iye, 24Pamenepo ndinapatula akulu a ansembe khumi ndi awiri,
ndiwo Serebiya, Hasabiya, ndi abale ao khumi pamodzi nao, 25ndi
kuwayesera siliva, ndi golidi, ndi zipangizo, ndizo copereka ca kwa
nyumba ya Mulungu wathu, cimene mfumu, ndi aphungu ace, ndi
akalonga ace, ndi Aisrayeli onse anali apawa, adapereka. 26Ndipo
ndinawayesera m'dzanja mwao matalente a siliva mazana asanu
ndi limodzi mphambu makumi asanu, ndi zipangizo zasiliva
matalente zana limodzi, 27ndi zikho zagolidi makumi awiri za
madariki cikwi cimodzi, ndi zipangizo ziwiri za mkuwa wabwino
wonyezimira wokhumbika ngati golidi. 28Ndipo ndinanena nao, Inu
ndinu opatulikira Yehova, ndi zipangizozo nzopatulikira, ndi siliva
ndi golidi, ndizo copereka caufulu ca kwa Yehova Mulungu wa
makolo anu. 29Mukhale maso ndi kuzisunga mpaka muziyesera
pamaso pa akulu a ansembe ndi Alevi, ndi akulu a nyumba za
makolo a Israyeli ku Yerusalemu, m'zipinda za nyumba ya
Yehova. 30Potero ansembe ndi Alevi analandira kulemera kwace
kwa siliva ndi golidi ndi zipangizo, abwere nazo ku Yerusalemu ku
nyumba ya Mulungu wathu.
31Pamenepo tinacoka ku mtsinje wa Ahava tsiku lakhumi ndi ciwiri
la mwezi woyamba, kumka ku Yerusalemu; ndipo dzanja la
Mulungu wathu linakhala pa ife, ndi kutilanditsa m'dzanja la mdani
ndi wolalira m'njira. 32Ndipo tinafika ku Yerusalemu ndi kukhalako
masiku atatu. 33Ndi pa tsiku lacinai siliva ndi golidi ndi zipangizo
zinayesedwa m'nyumba ya Mulungu wathu, m'dzanja la Meremoti
mwana wa Uliya wansembe, ndi pamodzi naye Eleazara mwana wa
Pinehasi, ndi pamodzi nao Yozabadi mwana wa Yesuwa, ndi
Nowadia mwana wa Binui, Alevi; 34zonsezi anaziwerenga ndi
kuziyesa; ndi kulemera kwace konse kunalembedwa nthawi
yomweyo. 35Otengedwa ndende, ataturuka m'ndende, anapereka
nsembe zopsereza kwa Mulungu wa Israyeli, ng'ombe khumi ndi
ziwiri za Aisrayeli onse, nkhosa zamphongo makumi asanu ndi anai
mphambu zisanu ndi imodzi, ana a nkhosa makumi asanu ndi awiri
mphambu asanu ndi awiri, atonde khumi ndi awiri, akhale nsembe
yazolakwa; zonsezi ndizo nsembe yopsereza ya kwa
Yehova. 36Ndipo anapereka malamulo a mfumu kwa akazembe a

mfumu, ndi kwa ziwanga, tsidya lino la mtsinjewo; ndipo iwo anathandiza anthu ndi nyumba ya Mulungu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Ezara 9

Mwankhawa Ezara apempherera Ayuda okwatira acilendo kwa Mulunzu

1Zitatha izi tsono anandiyandikira akalonga, ndi kuti, Anthu a
Israyeli, ndi ansembe, ndi Alevi, sanadzilekanitsa ndi anthu a
maikowa, kunena za zonyansa zao za Akanani, Ahiti, Aperizi,
Ayebusi, Aamoni, Amoabu, Aaigupto, ndi Aamori. 2Pakuti
anadzitengera okha ndi ana amuna ao ana akazi ao; nisokonezeka
mbeu yopatulika ndi mitundu ya maikowa; inde dzanja la akalonga
ndi olamulira linayamba kulakwa kumene. 3Ndipo pakumva mau
awa ndinang'amba cobvala canga, ndi maraya anga, ndi
kumwetula tsitsi la pamutu panga ndi ndebvu zanga, ndi kukhala
pansi m'kudabwa. 4Nandisonkhanira ali yense wakunjenjemera pa
mau a Mulungu wa Israyeli, cifukwa ca kulakwa kwa iwo a ndende;
ndipo ndinakhala m'kudabwa mpaka nsembe yamadzulo. 5Ndi pa
nsembe yamadzulo ndinanyamuka m'kuzunzika kwanga, cobvala
canga ndi maraya anga zong'ambika; ndipo ndinagwada ndi
maondo anga, ndi kutambasula manja anga kwa Yehova Mulungu
wanga; 6ndipo ndinati, Mulungu wanga, ndigwa nkhope, ndi kucita
manyazi kuweramutsa nkhope yanga kwa inu Mulungu wanga,
popeza mphulupulu zathu zacuruka pamtu pathu, ndi kuparamula
kwathu kwakula kufikira m'Mwamba. 7Ciyambire masiku a makolo
athu taparamula kwakukuru mpaka lero lino; ndi cifukwa ca
mphulupulu zathu ife, mafumu athu, ndi ansembe athu,
tinaperekedwa m'dzanja la mafumu a maikowo, kulupanga
kundende, ndi kufunkhidwa, ndi kucitidwa manyazi pankhope
pathu, monga lero lino. 8Ndipo tsopano, kamphindi, Yehova
Mulungu wathu wationetsa cisomo, kutisiyira cipulumutso, ndi
kutipatsa ciciri m'malo mwace mopatulika; kuti Mulungu wathu
atipenyetse m'maso mwathu, ndi kutitsitsimutsa pang'ono
m'ukapolo wathu. 9Popeza ife ndife akapolo, koma Mulungu wathu
sanatisiya m'ukapolo wathu, natifikitsira cifundo pamaso pa
mafumu a Perisiya, kuti atitsitsimutse kuimika nyumba ya Mulungu
wathu, ndi kukonzanso muunda wace, ndi kutipatsa linga m'Yuda
ndi m'Yerusalemu. 10Ndipo tsopano, Mulungu wathu, tidzanenanji
pambuyo pa ici? pakuti tasiya malamulo anu, 11amene
munalamulira mwa atumiki anu aneneri ndi kuti, Dzikolo
mumukako likhale colowa canu ndilo dziko lodetsedwa mwa
cidetso ca anthu a m'maikomo, mwa zonyansa zao zimene
zinalidzaza, kuyambira nsonga yina kufikira nsonga inzace ndi ucisi
wao. 12Cifukwa cace tsono, musamapereka ana anu akazi kwa ana
ao amuna, kapena kutengera ana anu amuna ana ao akazi, kapena
kufuna mtendere wao ndi kukoma kwao nthwawi yonse, kuti
mukhale olimba, ndi kudya zokoma za m'dziko, ndi kulisiyira ana

anu colowa ca ku nthawi yonse. 13Ndipo zitatigwera zonsezi
cifukwa ca nchito zathu zoipa ndi kuparamula kwathu kwakukuru;
popeza inu Mulungu wathu mwatilanga moticepsera mphulupulu
zathu, ndi ku tipatsa cipulumutso cotere; 14kodi tidzabwereza
kuphwanya malamulo anu, ndi kukwatana nayo mitundu ya anthu
ocita zonyansa izi? Simudzakwiya nafe kodi mpaka mwatitha, ndi
kuti pasakhale otsala kapena akupulumuka? 15Yehova Mulungu wa
Israyeli, Inu ndinu wolungama, popeza tinatsala opulumuka monga
lero lino; taonani, tiri pamaso panu m'kuparamula kwathu; pakuti
palibe wakuima pamaso panu cifukwa ca ici.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Ezara 10

Acotsedwa akazi acilendo

1Pakupemphera Ezara tsono, ndi kuulula ndi kulira misozi, ndi
kudzigwetsa pansi pakhomo pa nyumba ya Mulungu,
udamsonkhanira mwa Israyeli msonkhano waukuru ndithu wa
amuna, ndi akazi, ndi ana; popeza anthu analira kulira,
kwakukuru. 2Pamenepo Sekaniya mwana wa Yehiyeli, mwana wina
wa Elamu, anambwezera Ezara mau, nati, Talakwira Mulungu
wathu, tadzitengera akazi acilendo a mitundu ya dzikoli; koma
tsopano cimtsalira Israyeli ciyembekezo kunena za cinthu
ici. 3Ndipo tsono tipangane ndi Mulungu wathu kucotsa akazi onse,
ndi obadwa mwa iwo, monga mwa uphungu wa mbuye wanga, ndi
wa iwo akunjenjemera pa lamulo la Mulungu wathu; ndipo cicitike
monga mwa cilamulo. 4Nyamukani, mlandu ndi wanu; ndipo ife tiri
nanu; limbikani, citani. 5Nanyamuka Ezara, nalumbiritsa akulu a
ansembe, ndi Alevi, ndi Aisrayeli onse, kuti adzacita monga mwa
mau awa. Nalumbira iwo. 6Pamenepo Ezara ananyamuka pakhomo
pa nyumba ya. Mulungu, nalowa m'cipinda ca Yehohanana mwana
wa Eliyasibu, ndipo atafikako sanadya mkate, sanamwa madzi;
pakuti anacita maliro cifukwa ca kulakwa kwa iwo otengedwa
ndende. 7Nabukitsa iwo mau mwa Yuda ndi Yerusalemu kwa ana
onse otengedwa ndende, kuti azisonkhana ku Yerusalemu; 8ndi kuti
ali yense wosafikako atapita masiku atatu, monga mwa uphungu
wa akalonga ndi akuru, cuma cace conse cidzaonongeka konse,
ndipo iye adzacotsedwa ku msonkhano wa iwo otengedwa
ndende. 9Ndipo anasonkhana ku Yerusalemu amuna onse a Yuda
ndi Benjamini asanapite masiku atatu, ndiwo mwezi wacisanu ndi
cinai, tsiku la makumi awiri a mwezi; nakhala pansi anthu onse
m'khwalala pakhomo pa nyumba ya Mulungu, alikunjenjemera
cifukwa ca mlandu uwu, ndi cifukwa ca mvulayi. 10Pamenepo Ezara
wansembe ananyamuka, nanena nao, Mwalakwa, mwadzitengera
akazi acilendo, kuonjezera kuparamula kwa Israyeli. 11Cifukwa
cace tsono, ululani kwa Yehova Mulungu wa makolo anu, nimucite
comkondweretsa; mudzilekanitse ndi mitundu ya anthu a
m'dzikomo, ndi kwa akazi acilendo. 12Ndipo unayankha msonkhano
wonse, ndi kunena ndi mau akuru, Monga mwa mau anu tiyenera
kucita. 13Koma anthu ndiwo ambiri, ndi nyengo yino nja mvula,
tiribenso mphamvu yakuima pabwalo, ndi nchitoyi sindiyo ya tsiku
limodzi kapena awiri; pakuti tacurukitsa kulakwa kwathu pa cinthu
ici. 14Ayang'anire ici tsono akalonga athu a msonkhano wonse, ndi
onse a m'midzi mwathu amene anadzitengera akazi acilendo
abwere pa nthawi zoikika, ndi pamodzi nao akuru a mudzi wao uli
wonse, ndi oweruza ace, mpaka udzaticokera mkwiyo waukali wa
Mulungu wathu cifukwa ca mlandu uwu. 15Yonatani mwana wa

Asaheli ndi Yazeya mwana wa Tikiva okha anatsutsana naco, ndi
Mesulamu ndi Sabetai Mlevi anawathandiza. 16Pamenepo anthu
otengedwa ndende anacita cotero. Ndi Ezara wansembe, ndi anthu
akuru a nyumba za makolo, monga mwa nyumba za makolo ao,
iwo onse ochulidwa maina ao anasankhidwa, nakhala pansi tsiku
loyamba la mwezi wakhumi kufunsa za mlanduwu. 17Natsiriza nao
amuna onse adadzitengera akazi acilendo tsiku loyamba la mwezi
woyamba. 18Ndipo anapeza mwa ana a ansembe odzitengera akazi
acilendo, ndiwo a ana a Yesuwa mwana wa Yozadaki, ndi abale ace
Maseya, ndi Eliezere, ndi Yaribu, ndi Gedaliya. 19Ndipo anaimika
dzanja lao kuti adzacotsa akazi ao; ndipo popeza adaparamuladi,
anapereka nsembe nkhosa yamphongo ya zoweta pa kuparamula
kwao. 20Ndi a ana a Imeri: Hanani ndi Zebadiya. 21Ndi a ana a
Harimu: Maseya, ndi Eliya, ndi Semaya, ndi Yehiyeli, ndi
Uziya. 22Ndi a ana a Pasuru: Elioenai, Maseya, Ismayeli, Netaneli,
Yozabadi, ndi. Elasa. 23Ndi a Alevi: Yozabadi, ndi Simei, ndi Kelaya
(ndiye Kelita), Petahiya, Yuda, ndi Eliezere. 24Ndi a oyimbira:
Eliasibu; ndi a odikira: Salumu, ndi Telemu, ndi Uri. 25Ndi Aisrayeli
a ana a Parosi: Ramiya, ndi Iziya, ndi Matikiya, ndi Miyamini, ndi
Eleazara, ndi Malikiya, ndi Benaya. 26Ndi a ana a Elamu: Mataniya,
Zekariya, ndi Yehieli, ndi Abidi, ndi Yeremoti, ndi Eliya. 27Ndi a ana
a Zatu: Elioenai, Eliasibi, Mataniya, ndi Yeremoti, ndi Zabadi, ndi
Aziza. 28Ndi a ana a Bebai: Yehohanana, Hananiya, Zabai,
Atilai. 29Ndi a ana a Bani: Mesulamu, Makuli, ndi Adaya, Yasubi, ndi
Seali, Yeremoti. 30Ndi a ana a Pahati: Moabu, Adina, ndi Kelali,
Benaya, Maseya, Mataniya, Bezaleli, ndi Binui, ndi Manase. 31Ndi a
ana a Harimu: Eliezere, Isiya, Malikiya, Semaya,
Simeoni, 32Benjamini, Maluki, Semariya. 33A ana a Hasumu:
Matenai, Matata. Zabadi, Elifeleti, Yeremai, Manase, Simei. 34A ana
a Bani: Madai, Amiramu, ndi Ueli, 35Benaya, Bedeya,
Kelui, 36Vaniya, Meremoti, Eliasibi, 37Mataniya, Matenai, ndi
Yasu, 38ndi Bani, ndi Binui, Simei, 39ndi Selemiya, ndi Natani, ndi
Adaya, 40Makinadebai, Sasai, Sarai, 41Azareli, ndi Seleimiya,
Semariya, 42Salumu, Amariya, Yosefe. 43A ana a Nebo: Yeieli,
Matitiya, Zabadi, Zebina, Ido, ndi Yoeli, Banaya, 44Awa onse
adatenga akazi acilendo, ndi ena a iwowa anali ndi akazi amene
adawabalira ana.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Nehemiah

Nehemiya 1

Nehemiya apempherera ana a Israyeli kwa Mulungu

1MAU a Nehemiya mwana wa Hakaliya. Kunali tsono mwezi wa
Kisilevi, caka ca makumi awiri, pokhala ine ku Susani ku nyumba
ya mfumu, 2anafika Hanani, mmodzi wa abale anga, iye ndi amuna
ena a ku Yuda; ndipo ndinawafunsa za Ayuda adapulumukawo
otsala andende, ndi za Yerusalemu. 3Nanena nane iwo, Otsalawo
otsala andende uko ku dzikoko akulukutika kwakukuru,
nanyozedwa; ndi linga la Yerusalemu lapasuka, ndi zipata zace
zatenthedwa ndi moto. 4Ndipo kunali, pakumva'mau awa,
ndinakhala pansi ndi kulira misozi, ndi kucita maliro masiku ena,
ndinasalanso, ndi kupemphera pamaso pa Mulungu wa
Kumwamba, 5ndi kuti, Ndikupembedzani Yehova, Mulungu wa
Kumwamba, Mulungu wamkuru ndi woopsa, wakusunga pangano
ndi cifundo ndi iwo akumkonda ndi kusunga malamulo
ace; 6muchere khutu, ndi maso anu atseguke kumvera pemphero
la kapolo wanu, ndilipempha pamaso panu tsopano apa msana ndi
usiku, kupempherera ana a Israyeli akapolo anu, ndi kuulula zoipa
za ana a Israyeli zimene tacimwira nazo Inu; inde tacimwa, ine ndi
nyumba ya atate wanga. 7Tacita mwamphulupulu pa Inu, osasunga
malamulo, kapena malemba, kapena maweruzo, amene
mudalamulita mtumiki wanu Mose. 8Mukumbukile mau
mudalamulira mtumiki wanu Mose, ndi kuti, Mukalakwa,
ndidzakubalalitsani mwa mitundu ya anthu; 9koma mukabwerera
kudza kwa Ine, ndi kusunga malamulo anga, ndi kuwacita,
angakhale otayika anu anali ku malekezero a thambo,
ndidzawasonkhanitsa kucokera komweko, ndi kubwera nao ku
malo ndinawasankha kukhalitsako dzina langa. 10Ndipo awa ndi
akapolo anu ndi anthu anu, amene munawaombola ndi mphamvu
yanu yaikuru, ndi dzanja lanu lolimba. 11Yehova, mucherere khutu
pemphero la kapolo wanu, ndi pemphero la akapolo anu
okondwera nako kuopa dzina lanu; ndipo mulemereze kapolo wanu
lero lino, ndi kumuonetsera cifundo pamaso pa munthu uyu. Koma
ndinali ine wothirira mfumu cakumwa cace.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Aritasasta alola Nehemiya akamange linga la Yerusalemu

1Koma kunacitika mwezi wa Nisana, caka ca makumi awiri ca
Aritasasta mfumu pokhala vinyo pamaso pace, ndinatenga vinyoyo
ndi kuipatsa mfumu. Koma sindidakhala wacisoni pamaso pace ndi
kale lonse. 2Ninena nane mfumu, Nkhope yako nja cisoni cifukwa
ninji popeza sudwala? ici si cinthu cina koma cisoni ca mtima.
Pamenepo ndinacita mantha akuru. 3Ndipo ndinati kwa mfumu,
Mfumu ikhale ndi moyo kosatha; ilekerenji nkhope yanga kucita
cisoni, popeza pali bwinja kumudzi kuli manda a makolo anga, ndi
zipata zace zopsereza ndi moto. 4Ndipo mfumu inati kwa ine,
Ufunanji iwe? Pamenepo ndinapemphera Mulungu wa
Kumwamba. 5Ndipo ndinati kwa mfumu, Cikakomera mfumu, ndi
mtima wanu ukakomera kapolo wanu, munditumize ku Yuda ku
mudzi wa manda a makolo anga, kuti ndiumange. 6Ninena nane
mfumu, irikukhala pansi pamodzi ndi mkazi wace wamkuru, Ulendo
wako ngwa nthawi yanji, udzabweranso liti? Ndipo kudakonda
mfumu kunditumiza nditaichula nthawi. 7Ndinanenanso kwa
mfumu, Cikakomera mfumu, indipatse akalata kwa ziwanga za
tsidya lija la mtsinje, andilole ndipitirire mpaka ndifikira ku
Yuda; 8ndi kalata kwa Asafu wosunga misitu ya mfumu, kuti
andipatse mitengo ya mitanda ya ku zipata, za linga liri kukacisi,
ndi ya linga la mudzi, ndi ya nyumba imene ndidzalowamo ine.
Ndipo mfumu inandipatsa monga mwa dzanja lokoma la Mulungu
londikhalira. 9Ndinafika tsono kwa ziwanga za tsidya lino la
mtsinje, ndipo ndinawapatsa akalata a mfumu. Koma mfumu
idatumiza apite nane akazembe a nkhondo, ndi
apakavalo. 10Atamva Sanibalati Mhoroni, ndi Tobiya kapoloyo M-
amoni, cidawaipira kwakukuru, kuti wadza munthu kuwafunica ana
a Israyeli cokoma. 11Motero ndinafika ku Yerusalemu, ndi
kukhalako masiku atatu. 12Ndipo ndinauka usiku, ine ndi amuna
owerengeka nane, osauza munthu yense ine coika Mulungu wanga
m'mtima mwanga ndicitire Yerusalemu; panalibenso nyama yina
nane, koma nyama imene ndinakhalapo. 13Ndipo ndinaturuka
usiku pa cipata ca kucigwa, kumka ku citsime ca cinjoka, ndi ku
cipata ca kudzala, ndi kuyang'ana malinga a Yerusalemu
adapasukawo, ndi zipata zace zothedwa ndi moto. 14Ndipo
ndinapitima kumka ku cipata cacitsime, ndi ku dziwe la mfumu;
koma popita nyama iri pansi panga panaicepera. 15Ndipo
ndinakwera usiku kumtsinje, ndi kuyang'ana lingali; ndinabwerera
tsono ndi kulowa pa cipata ca kucigwa, momwemo
ndinabwereranso. 16Koma olamulira sanadziwa uko ndinamuka,
kapena cocita ine; sindidauzenso kufikira pamenepo Ayuda,
kapena ansembe, kapena aufuru, kapena olamulira, kapena otsala

akucita nchitoyi. 17Pamenepo ndinanena nao, Muona coipa
m'mene tirimo, kuti Yerusalemu ali bwinja, ndi zipata zace
zotentha ndi moto; tiyeni, timange linga la Yerusalemu,
tisakhalenso cotonzedwa. 18Ndinawauzanso za dzanja la Mulungu
wanga londikhalira mokoma, ndiponso za mau anandiuza mfumu.
Nati iwo, Tinyamuke, timange. Cotero anandilimbitsira manja
mokoma. 19Koma Sanibalati Mhoroni, ndi Tobiya kapolo M-amoniyo,
ndi Gesemu M-arabu, anamva natiseka pwepwete, natipeputsa,
nati, Ciani ici mucicita? Mulikupandukira mfumu kodi? 20Koma
ndinawabwezera mau, ndi kunena nao, Mulungu Wam'mwamba,
Iye ndiye adzatilemeza; cifukwa cace ife akapolo ace
tidzanyamuka ndi kumanga; koma inu mulibe gawo, kapena
ulamuliro, kapena cikumbukilo, m'Yerusalemu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Mamangidwe a malinga ndi zipata za Yerusalemu

1Pamenepo Eliasibu mkuru wa ansembe ananyamuka pamodzi ndi
abale ace ansembe, namanga cipata cankhosa; anacipatula, naika
zitseko zace, inde anacipatula mpaka nsanja ya Mea, mpaka
nsanja ya Hananeeli. 2Ndi pambali pace anamanga amuna a ku
Yeriko. Ndi pambali pao anamanga Zakuri mwana wa Imri. 3Ndi
cipata cansomba anacimanga ana a Hasenaa; anamanga mitanda
yace, ndi kuika zitseko zace, zokowera zace, ndi mipingiridzo
yace. 4Ndi pambali pao anakonza Meremoti mwana wa Uliya,
mwana wa Kozi. Ndi pambali pao anakonza Mesulamu mwana wa
Berekiya, mwana wa Mesezabele. Ndi pambali pao anakonza
Zadoki mwana wa Baana. 5Ndi pambali pao anakonza Atekoa;
koma omveka ao sanapereka makosi ao ku nchito ya Mbuye
wao. 6Ndi cipata cakale anacikonza Yoyada mwana wa Paseya; ndi
Mesulamu mwana wa Besodeya anamanga mitanda yace, ndi
kuika zitseko zace, ndi zokowera zace, ndi mipingiridzo yace. 7Ndi
pambali pao anakonza Melatiya Mgibeoni, ndi Yadoni Mheronoti,
ndi amuna a ku Gibeoni, ndi a ku Mizipa, wa ulamuliro wa ciwanga
tsidya lino la mtsinje. 8Pambali pace anakonza Uziyeli mwana wa
Haraya, wa iwo osula golidi. Ndi padzanja pace anakonza
Hananiya, wa iwo osanganiza zonunkhira; nalimbikitsa Yerusalemu
mpaka linga lacitando. 9Ndi pambali pao anakonza Refaya mwana
wa Huri, ndiye mkuru wa dera lina la dziko la Yerusalemu. 10Ndi
pambali pao anakonza Yedaya mwana wa Harumafi, pandunji pa
nyumba yace. Ndi pambali pace anakonza Hatusi mwana wa
Hasabineya. 11Malikiya mwana wa Harimu, ndi Hasubi mwana wa
Pahati-Moabu, anakonzal gawo lina, ndi nsanja ya ng'anjo. 12Ndi
pambali pace anakonza Salumu mwana wa Halohesi, mkuru wa
dera lina la dziko la Yerusalemu, iye ndi ana ace akazi. 13Cipata ca
kucigwa anacikonza Hanini; ndi okhala m'Zanowa anacimanga,
naika zitseko zace, zokowera zace, ndi mipiringidzo yace; ndiponso
mikono cikwi cimodzi ca lingalo mpaka ku cipata ca kudzala. 14Ndi
cipata ca kudzala anacikonza Malikiya mwana wa Rekabu, mkuru
wa dziko la Bete Hakeremu; anacimanga, naika zitseko zace,
zokowera zace, ndi mipiringidzo yace. 15Ndi cipata ca kukasupe
anacikonza Saluni mwana wa Koli, Hoze mkuru wa dziko la Mizipa
anacimanga, nacikomaniza pamwamba pace, naika zitseko zace,
zokowera zace, ndi mipiringidzo yace; ndiponso linga la dziwe la
Sela pa munda wa mfumu, ndi kufikira ku makwerero otsikira ku
mudzi wa Davide. 16Potsatizana naye anakonza Nehemiya mwana
wa Azibuki, mkuru wa dera lace lina la dziko la Bete Zuri, mpaka
malo a pandunji pa manda a Davide, ndi ku dziwe adalikumba, ndi
ku nyumba ya amphamvu aja. 17Potsatizana naye anakonza Alevi,

Rehumu mwana wa Bani. Pambali pace anakonza Hasabiya mkuru
wa dera lina la dziko la Keila, kukonzera dziko lace. 18Potsatizana
naye anakonza abale ao, Bavai mwana wa Henadadi, mkuru wa
dera lina la dziko la Keila. 19Ndi pa mbali pace Ezeri mwana wa
Yesuwa, mkuru wa Mizipa, anakonza gawo lina, pandunji
pokwerera ku nyumba yosungamo zida za nkhondo, popindirira
linga. 20Potsatizana naye Baruki mwana wa Zabai anafulumira
kukonza gawo lina kuyambira popindirira mpaka ku khomo la
nyumba ya Eliasibu mkuru wa ansembe. 21Potsatizana naye
Meremoti mwana wa Uliya mwana wa Hakozi anakonza gawo lina,
kuyambira ku khomo la nyumba ya Eliasibu kufikira malekezero
ace a nyumba ya Eliasibu. 22Ndi potsatizana naye anakonza
ansembe okhala kucidikha. 23Potsatizana nao anakonza Benjamini
ndi Hasubi pandunji pa nyumba pao, Potsatizana nao anakonza
Azariya mwana wa Maseya mwana wa Ananiya pafupi pa nyumba
yace. 24Potsatizana naye Binui mwana wa Henadadi anakonza
gawo lina, kuyambira ku nyumba ya Azariya kufikira popindirira
kufikira kungondya. 25Palali mwana wa Uzai anakonza pandunji
popindirira, ndi nsanja yosomphoka pa nyumba ya mfumu ya
kumtunda, imene iri ku bwalo la kaidi. Potsatizana naye anakonza
Pedaya mwana wa Parosi. 26Koma Anetini okhala m'Ofeli anakonza
kufikira ku malo a pandunji pa cipata ca kumadzi kum'mawa, ndi
nsanja yosomphokayo, 27Potsatizana nao Atekoa anakonza gawo
lina, pandunji pa nsanja yaikuru yosomphoka ndi ku linga la
Ofeli. 28Kumtunda kwa cipata ca akavalo anakonza ansembe,
yense pandunji pa nyumba yace. 29Potsatizana nao anakonza
Zadoki mwana wa Imeri pandunji pa nyumba yace. Ndi potsatizana
naye anakonza Semaya mwana wa Sekaniya, wosunga cipata ca
kum'mawa. 30Potsatizana naye Hananiya mwana wa Selemiya, ndi
Hanuni mwana wacisanu ndi cimodzi wa Salafi, anakonza gawo
lina. Potsatizana naye anakonza Mesulamu mwana wa Berekiya
pandunji pa cipinda cace. 31Potsatizana naye anakonza Malikiya
wina wa osula golidi kufikira ku nyumba ya Anetini, ndi ya ocita
malonda, pandunji pa cipata ca Hamifikadi, ndi ku cipinda cosanja
ca kungondya. 32Ndi pakati pa cipinda cosanja ca kungondya ndi
cipata cankhosa anakonza osula golidi ndi ocita malonda.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Adani ayesa kuwaletsa kumanga malinga

1Ndipo kunali, atamva Sanibalati kuti tinalikumanga lingali,
kudamuipira, nakwiya kwakukuru, naseka Ayuda
pwepwete. 2Nanena iye pamaso pa abale ace ndi ankhondo a ku
Samariya, nati, Alikucitanji Ayuda ofokawa? adzimangire linga
kodi? adzapereka nsembe kodi? adzatsiriza tsiku limodzi kodi?
adzakometsanso miyala ya ku miunda yotenthedwa? 3Ndipo Tobiya
M-amoni anali naye, nati, Cinkana ici acimanga, ikakwerako
nkhandwe, idzagamula linga lao lamiyala. 4Imvani, Mulungu
wathu, popeza tanyozeka ife; muwabwezere citonzo cao pamtu
pao, ndi kuwapereka akhale cofunkhidwa m'dziko la
ndende; 5ndipo musakwirira mphulupulu yao, ndi kulakwa kwao
kusafafanizike pamaso panu; pakuti anautsa mkwiyo wanu pamaso
pa omanga linga. 6Koma tinamanga lingali, ndi linga lonse
linalumikizana kufikira pakati mpakati; popeza mitima ya anthu
inalunjika kunchito.
7Koma kunali, atamva Sanibalati, ndi Tobiya, ndi Aarabu, ndi
Aamoni, ndi Aasidodi, kuti makonzedwe a malinga a Yerusalemu
anakula, ndi kuti mopasuka mwace munayamba kutsekeka,
cidawaipira kwambiri; 8napangana ciwembu iwo onse pamodzi,
kudzathira nkhondo ku Yerusalemu, ndi kucita cisokonezo
m'menemo. 9Koma tinapemphera kwa Mulungu wathu, ndi
kuwaikira olindirira usana ndi usiku, cifukwa ca iwowa. 10Ndipo
Ayuda anati, Mphamvu ya osenza akatundu yatha, ndi dothi
licuruka, motero sitidzakhoza kumanga lingali. 11Nati adani athu,
Sadzadziwa kapena kuona mpaka talowa pakati pao, ndi kuwapha,
ndi kuleketsa nchitoyi. 12Ndipo kunali, atafika Ayuda okhala pafupi
pao ocokera pamalo ponse, anatiuza ife kakhumi, Bwererani kwa
ife.

Ankhondo acinjiriza anchito

13Cifukwa cace ndinawaika potera m'kati mwa linga, popenyeka;
inde ndinaika anthu monga mwa mabanja ao, akhale nao
malupanga ao, nthungo zao, ndi mauta ao. 14Ndipo ndinapenya,
ndinanyamuka, ndinanena kwa aufulu, ndi olamulira, ndi anthu
otsala, Musamawaopa iwo; kumbukilani Yehova wamkuru ndi
woopsa, ndi kuponyera nkhondo abale anu, ana anu amuna ndi
akazi, akazi anu, ndi nyumba zanu. 15Ndipo kunali, pakumva adani
athu kuti cinadziwika nafe, ndi kuti Mulungu adapititsa pacabe
uphungu wao, tinabwera tonse kumka kulinga, yense ku nchito
yace. 16Ndipo kuyambira pamenepo gawo lina la anyamata anga
anagwira nchito, ndi gawo ina linagwira nthungo, zikopa, ndi
mauta, ndi maraya acitsulo; ndi akuru anali m'mbuyo mwa
nyumba yonse ya Yuda. 17Iwo omanga linga, ndi iwo osenza

katundu, posenza, anacita ali yense ndi dzanja lace lina logwira nchito, ndi lina logwira cida; 18ndi omanga linga ali yense anamangirira lupanga lace m'cuuno mwace, nagwira nchito motero. Ndipo woomba lipenga anali ndi ine. 19Ndipo ndinati kwa aufulu, ndi olamulira, ndi anthu otsala, Nchito ndiyo yocuruka ndi yacitando, ndi ife tiri palace palace palingapo, yense azana ndi mnzace; 20pali ponse mukumva mau a lipenga, musonkhanire komweko kwa ife; Mulungu wathu adzatigwirira nkhondo. 21Momwemo tinalikugwira nchito; gawo lina la iwo linagwira nthungo kuyambira mbanda kuca mpaka zaturuka nyenyezi. 22Ndinanenanso kwa anthu nthawi yomweyi, Ali yense agone m'Yerusalemu pamodzi ndi mnyamata wace, kuti atilindirire usiku, ndi kugwira nchito usana. 23Ndipo ine, ndi abale anga, ndi anyamata anga, angakhale amuna olindirira onditsata ine, nnena mmodzi yense wa ife anabvula zobvala zace, yense anapita ndi cida cace kumadzi.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Nehemiya acinjiriza aumphawi opsinjika

1Pamenepo panamveka kulira kwakukuru kwa anthu ndi akazi ao
kudandaula pa abale ao Ayuda. 2Popeza panali ena akuti, Ife, ana
athu amuna ndi akazi, ndife ambiri; talandira tirigu, kuti tidye
tikhale ndi moyo. 3Panali enanso akuti, Tirikupereka cikole minda
yathu, ndi minda yathu yampesa ndi nyumba zathu; kuti tilandire
tirigu cifukwa ca njalayi. 4Panali enanso akuti, Takongola ndarama
za msonkho wa mfumu; taperekapo cikole minda yathu, ndi minda
yathu yampesa. 5Koma tsopano thupi lathu likunga thupi la abale
athu, ana athu akunga ana ao; ndipo taonani, titengetsa ana athu
amuna ndi akazi akhale akapolo, ndi ana athu akazi ena
tawatengetsa kale; ndipo tiribe ife mphamvu ya kucitapo kanthu;
ndi minda yathu, ndi minda yathu yampesa, nja ena. 6Ndipo
pakumva kulira kwao, ndi mau ao, kunandiipira
kwambiri. 7Pamenepo mtima wanga unandipangira; ndipo
ndinatsutsana nao aufuru ndi olamulira, ndi kunena nao,
Mukongoletsa mwa phindu yense kwa mbale wace. Ndipo
ndinasonkhanitsa msonkhano waukuru wakuwatsutsa. 8Ndipo
ndinanena, nao, Ife monga umo tinakhoza, tinaombola abale athu
Ayuda ogulitsidwa kwa amitundu; ndipo kodi inu mukuti mugulitse
abale anu, kapena tiwagule ndi ife? Pamenepo anakhala du,
nasowa ponena. 9Ndinatinso, Cinthu mucitaci si cokoma ai;
simuyenera kodi kuyenda m'kuopa Mulungu wathu, cifukwa ca
mnyozo wa amitundu, ndiwo adani athu? 10Kodi ine, ndi abale
anga, ndi anyamata anga, tiwakongoletsa ndarama ndi tirigu mwa
phindu? Ndikupemphani, tileke phindu ili. 11Abwezereni lero lomwe
minda yao, minda yao yampesa, minda yao yaazitona, ndi nyumba
zao, ndi limodzi la magawo zana limodzi la ndarama, ndi tirigu,
vinyo, ndi mafuta, limene muwalipitsa. 12Pamenepo anati,
Tidzawabwezera osawalipitsa kanthu, tidzacita monga momwe
mwanena. Pamenepo ndinaitana ansembe, ndi kuwalumbiritsa,
kuti adzacita monga mwa mau awa. 13Ndinakutumulanso maraya
anga, ndi kuti, Mulungu akutumule momwemo munthu yense
wosasunga mau awa, ku nyumba yace, ndi ku nchito yace; inde
amkutumule momwemo, namtayire zace zonse. Ndi msonkhano
wonse unati, Amen, nalemekeza Yehova. Ndipo anthu anacita
monga mwa mau awa. 14Ndipo ciyambire tsiku lija anandiika
ndikhale kazembe wao m'dziko la Yuda; kuyambira caka ca
makumi awiri kufikira caka ca makumi atatu mphambu ziwiri ca
Aritasasta mfumu, ndizo zaka khumi ndi ziwiri, ine ndi abale anga
sitinadya cakudya ca kazembe. 15Koma akazembe akale
ndisanakhale ine, analemetsa anthu, nadzitengera kwa iwo mkate,
ndi vinyo, pamodzi ndi siliva masekeli makumi anai; angakale

anyamata ao anacita ufumu pa anthu; koma sindinatero ine, cifukwa ca kuopa Mulungu. 16Ndiponso ndinalimbikira nchito ya linga ili, ngakhale dziko sitinaligula, ndi anyamata anga onse anasonkhanira nchito komweko. 17Panalinso podyera ine Ayuda ndi olamulira amuna zana limodzi; mphambu makumi asanu, pamodzi ndi iwo akutidzera kucokera kwa amitundu otizinga. 18Zokonzekeratu tsiku limodzi tsono ndizo ng'ombe imodzi, ndi nkhosa zonenepa zisanu ndi imodzi, anandikonzeratunso nkhuku, ndi kamodzi atapita masiku khumi vinyo wambiri wa mitundu mitundu; cinkana conseci sindinafunsira cakudya ca kazembe, popeza ukapolo unalemerera anthuwo. 19Mundikumbukire Mulungu, zindikomere zonse ndinacitira anthu awa.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Adani ayesa kunyenga ndi kuopsa Nehemiya

1Kunali tsono, atamva Sanibalati, ndi Tobiya, ndi Gesemu M-arabu,
ndi adani athu otsala, kuti ndidatha kumanga lingali,
posatsalaponso popasuka; (ngakhale pajapo sindinaika zitseko
pazipata); 2anatumiza mau kwa ine Sanibalati ndi Gesemu, kuti,
Tiyeni tikomane ku midzi ya ku cigwa ca Ono; koma analingirira za
kundicitira coipa. 3Ndipo ndinawatumizira mithenga, ndi kuti,
Ndirikucita nchito yaikuru, sindikhoza kutsika; ndiidulirenji padera
nchito poileka ine, ndi kukutsikirani? 4Nanditumizira ine mau otere
kanai; ndinawabwezeranso mau momwemo. 5Pamenepo Sanibalati
anatuma mnyamata wace kwa ine kacisanu, ndi kalata wosatseka
m'dzanja mwace; 6m'menemo mudalembedwa, Kwamveka mwa
amitundu, ndi Gasimu acinena, kuti iwe ndi Ayuda mulikulingirira
za kupanduka; cifukwa cace mulikumanga lingali; ndipo iwe
udzakhala mfumu yao monga mwa mau awa. 7Ndiponso waika
aneneri akubukitsa za iwe ku Yerusalemu, ndi kuti, Ku Yuda kuli
mfumu, ndipo zidzamveka kwa mfumu, kuti kuli zotere. Tiyeni
tsono tipangane pamodzi. 8Koma ndinamtumizira mau, akuti,
Palibe zinthu zotere zonga unenazi, koma uzilingirira mumtima
mwako. 9Pakuti anafuna onse kutiopsa, ndi kuti, Manja ao adzaleka
nchito, ndipo siidzacitika. Koma Inu, Mulungu, mulimbitse manja
anga tsopano.
10Pamenepo ndinalowa m'nyumba ya Semaya mwana wa Delaya,
mwana wa Mehetabele, wobindikizidwayo, ndipo anati, Tikomane
ku nyumba ya Mulungu m'kati mwa Kacisi, titsekenso pa makomo
a Kacisi; pakuti akudza kudzapha iwe, inde akudza usiku kudzapha
iwe. 11Koma ndinati, Munthu ngati ine nkuthawa kodi? ndani
wonga ine adzalowa m'Kacisi kupulumutsa moyo wace?
sindidzalowamo. 12Ndipo ndinazindikira kuti sanamtuma Mulungu;
koma ananena coneneraco pa ine, popeza Tobiya ndi Sanibalati
adamlembera. 13Anamlembera cifukwa ca ici, kuti ine ndicite
mantha, ndi kucita cotero, ndi kucimwa; ndi kuti anditolerepo mbiri
yoipa ndi kundinyoza. 14Mukumbukile, Mulungu wanga, Tobiya ndi
Sanibalati monga mwa nchito zao izi, ndi Nowadiya mneneri
wamkazi yemwe, ndi aneneri otsala, amene anafuna kundiopsa.
15Ndipo linga linatsirizika pa tsiku la makumi awiri ndi lacisanu la
mwezi wa Eluli, titalimanga masiku makumi asanu mphambu
awiri. 16Ndipo kunali atacimva adani athu onse, amitundu onse
akutizinga anaopa, nagwadi nkhope; popeza anazindikira kuti
nchitoyi inacitika ndi Mulungu wathu. 17Masikuwo aufulu a Yuda
analemberanso akalata ambiri kwa Tobiya; ndipo anawafikanso
akalata ace a Tobiya. 18Pakuti ambiri m'Yuda analumbirirana naye
cibwenzi; popeza ndiye mkamwini wace wa Sekaniya mwana wa

Ara; ndi mwana wace Yehohanana adadzitengera mwana wamkazi wa Mesulamu mwana wa Berekiya. 19Anachulanso nchito zace zokoma pamaso panga namfotokozera iye mau anga. Ndipo Tobiya anatumiza akalata kuti andiopse ine.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Alonda adikira Yerusalemu

1Ndipo atatha kumanga linga, ndinaika zitseko, nakhazika odikira,
ndi oyimbira, ndi Alevi; 2ndipo ndinawapatsa mbale wanga Hanani,
ndi Hananiya kazembe wa kuboma, ulamuliro wa pa Yerusalemu;
popeza ndiye munthu wokhulupirika, naposa ambiri pakuopa
Mulungu. 3Ndinanenanso nao, Asatsegule pa zipata za Yerusalemu
lisanafunde dzuwa; ndi poimirira odikira atseke pazipata,
nimuzipiringidze, nimuike alonda mwa iwo okhala m'Yerusalemu,
yense polindirira pace, yense pandunji pa nyumba yace. 4Mudziwo
tsono ndi wacitando, ndi waukuru; koma anthu anali m'mwemo
ngowerengeka, nyumba zomwe sizinamangike.

Maina a oyamba kubwerera kucokera ku Babulo

5Ndipo Mulungu wanga anaika m'mtima mwanga kuti
ndiwasonkhanitse aufuru, ndi olamulira, ndi anthu, kuti
awerengedwe mwa cibadwidwe cao. Ndipo ndinapeza buku la
cibadwidwe la iwo adakwerako poyamba paja; ndinapeza
mudalembedwa m'mwemo. 6Ana a dziko amene anakwera
kucokera kundende a iwo adatengedwa ndende, amene
Nebukadinezara mfumu ya Babulo adawatenga, anabwera ku
Yerusalemu ndi ku Yuda, yense ku mudzi wace, ndi awa: 7ndiwo
amene anadza ndi Zerubabele: Yesuwa, Nehemiya, Azariya,
Raamiya, Nahamani, Moredekai, Bilisani, Misiperete, Bigivai,
Nehumu, Baana. Mawerengedwe a amuna a anthu Aisrayeli
ndiwo: 8ana a Parosi zikwi ziwiri mphambu zana limodzi kudza
makumi asanu ndi awiri. 9Ana a Sefatiya, mazana atatu mphambu
makumi asanu ndi awiri kudza awiri. 10Ana a Ara, mazana asanu
ndi limodzi mphambu makumi asanu kudza awiri. 11Ana a Pakati
Moabu, a ana a Yesuwa ndi Yoabu, zikwi ziwiri mphambu mazana
asanu ndi atatu kudza khumi limodzi ndi asanu ndi atatu. 12Ana a
Elamu, cikwi cimodzi mphambu mazana awiri ndi makumi asanu
kudza anai. 13Ana a Zatu, mazana asanu ndi atatu mphambu
makumi anai kudza asanu. 14Ana a Zakai, mazana asanu ndi awiri
mphambu makumi asanu ndi limodzi. 15Ana a Binui, mazana asanu
ndi limodzi mphambu makumi anai kudza asanu ndi atatu. 16Ana a
Betai, mazana asanu ndi limodzi mphambu makumi awiri kudza
asanu ndi atatu. 17Ana a Azigadi, zikwi ziwiri mphambu mazana
atatu kudza makumi awiri ndi awiri. 18Ana a Adonikamu, mazana
asanu ndi limodzi mphambu makumi asanu ndi limodzi, kudza
asanu ndi awiri. 19Ana a Bigivai, zikwi ziwiri mphambu makumi
asanu ndi limodzi kudza asanu ndi awiri. 20Ana a Adini, mazana
asanu ndi limodzi mphambu makumi asanu kudza asanu. 21Ana a
Aberi, a Hezekiya, makumi asanu ndi anai kudza asanu ndi
atatu. 22Ana a Hasumu, mazana atatu mphambu makumi awiri

kudza asanu ndi atatu. 23Ana a Bezai, mazana atatu mphambu makumi awiri kudza anai. 24Ana a Harifi, zana limodzi mphambu khumi ndi awiri. 25Ana a Gibeoni, makumi asanu ndi anai kudza asanu. 26Amuna a ku Betelehemu ndi ku Netofa, zana limodzi mphambu makumi asanu ndi atatu kudza asanu ndi atatu. 27Amuna a ku Anatoti, zana limodzi mphambu makumi awiri kudza asanu ndi atatu. 28Amuna a ku Bete-Azimaveti, makumi anai kudza awiri. 29Amuna a ku Kiriyati Yearimu, Kefiira, ndi Beeroti, mazana asanu ndi awiri mphambu makumi anai kudza atatu. 30Amuna a ku Rama ndi Geba, mazana asanu ndi limodzi mphambu makumi awiri kudza mmodzi. 31Amuna a ku Mikimasi, zana limodzi mphambu makumi awiri kudza awiri. 32Amuna a ku Betele ndi Ai, zana limodzi mphambu makumi awiri kudza atatu. 33Amuna a ku Nebo winayo, makumi asanu kudza awiri. 34Ana a Elamu winayo, cikwi cimodzi mphambu mazana awiri ndi makumi asanu kudza anai. 35Ana a Harimu, mazana atatu mphambu makumi awiri. 36Ana a Yeriko, mazana atatu mphambu makumi anai kudza asanu. 37Ana a Lodi, Hadidi, ndi Ono, mazana asanu ndi awiri mphambu makumi awiri kudza mmodzi. 38Ana a Senaa, zikwi zitatu mphambu mazana asanu ndi anai kudza makumi atatu. 39Ansembe: ana a Yedaya, a nyumba ya Yesuwa, mazana asanu ndi anai mphambu makumi asanu ndi awiri kudza atatu. 40Ana a Imeri, cikwi cimodzi mphambu makumi asanu kudza awiri. 41Ana a Pasuru, cikwi cimodzi mphambu mazana awiri kudza makumi anai ndi asanu ndi awiri. 42Ana a Harimu, cikwi cimodzi mphambu khumi limodzi kudza asanu ndi awiri. 43A Levi: ana a Yesuwa, a Kadimiyeli, a ana a Hodeva, makumi asanu ndi awiri kudza anai. 44Oyimbira: ana a Asafu, zana limodzi mphambu makumi anai kudza asanu ndi atatu. 45Odikira: ana a Salumu, ana a Ateri, ana a Talimoni, ana a Akubu, ana a Hatita, ana a Sobai, zana limodzi mphambu makumi atatu kudza asanu ndi atatu. 46Anetini: ana a Ziha, ana a Hasufa, ana a Tabaoti, 47ana a Kerosi, ana a Siya, ana a Padoni, 48ana a Lebana, ana a Hagaba, ana a Salimai, 49ana a Hanani, ana a Gideri, ana a Gahara, 50ana a Reaya, ana a Rezini, ana a Nekoda, 51ana a Gazamu, ana a Uza, ana a Paseya, 52ana a Besai, ana a Meunimu, ana a Nefusesimu, 53ana a Bakibuki, ana a Hakufa, ana a Harihuri, 54ana a Baziliti, ana a Mehida, ana a Harisa, 55ana a Barikosi, ana a Sisera, ana a Tema, 56ana a Neziya, ana a Hatifa. 57Ana a akapolo a Solomo: ana a Sotai, ana a Sofereti, ana a Perida, 58ana a Yaala, ana a Darikoni, ana a Gideli, 59ana a Sefatiya, ana a Hatili, ana a Pokereti Hazebaimu, ana a Amoni. 60Anetini onse, ndi ana a akapolo a Solomo, ndiwo mazana atatu mphambu makumi asanu ndi anai kudza awiri. 61Ndipo okwera kucokera ku Telemela,

Teleharisa, Kerubi, Adoni, ndi Imeri, ndi awa; koma sanakhoza
kuchula nyumba za makolo ao, kapena mbumba zao, ngati ali a
Israyeli; 62ana a Delaya, ana a Tobiya, ana a Nekoda, mazana
asanu ndi limodzi mphambu makumi anai kudza awiri. 63Ndi a
ansembe: ana a Hobaya, ana a Hokozi, ana a Barizilai, amene
anadzitengera mkazi wa ana akazi a Barizilai Mgileadi, nachedwa
ndi dzina lao. 64Awa anafunafuna maina ao m'buku la iwo
owerengedwa mwa cibadwidwe, koma osawapeza; potero
anawayesa odetsedwa, nawacotsa ku nchito ya nsembe. 65Ndipo
kazembe anawauza kuti asadyeko zopatulikitsa, mpaka wauka
wansembe wokhala ndi Urimu ndi Tumimu. 66Msonkhano wonse
pamodzi ndiwo zikwi makumi anai ndi ziwiri mphambu mazana
atatu kudza makumi asanu ndi limodzi, 67osawerenga akapolo ao
amuna ndi akazi, ndiwo zikwi zisanu ndi ziwiri mphambu mazana
atatu ndi makumi atatu kudza asanu ndi awiri; ndipo anakhala nao
amuna ndi akazi oyimbira mazana awiri mphambu makumi anai
kudza asanu ndi mmodzi. 68Akavalo ao ndiwo mazana asanu ndi
awiri mphambu makumi atatu kudza asanu ndi mmodzi; nyuru zao
mazana awiri mphambu makumi anai kudza zisanu 69ngamira zao
mazana anai mphambu makumi atatu kudza asanu aburu ao zikwi
zisanu ndi cimodzi mphambu mazana asanu ndi awiri kudza
makumi awiri.

Zopereka za akulu

70Ndipo ena a akuru a nyumba za makolo anapereka kunchito.
Kazembeyo anapereka kucuma madariki agolidi cikwi cimodzi,
mbale zawazira makumi asanu, maraya a ansembe makumi
atatu. 71Enanso a akuru a nyumba za makolo anapereka ku cuma
ca nchitoyi, madariki agolidi zikwi makumi awiri, ndi miyeso ya
siliva zikwi ziwiri mphambu mazana awiri. 72Zopereka za anthu
otsala ndizo madariki agolidi zikwi makumi awiri, ndi miyeso ya
siliva zikwi ziwiri, ndi maraya a ansembe makumi asanu ndi limodzi
mphambu asanu ndi awiri. 73Nakhala m'midzi mwao ansembe, ndi
Alevi, ndi odikira, ndi oyimbira, ndi anthu ena, ndi Anetini, ndi
Aisrayeli onse.

Utakhala tsono mwezi wacisanu ndi ciwiri ana a Israyeli anakhala
m'midzi mwao.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Ezara awerengera anthu buku la cilamulo

1Ndipo anthu onse anasonkhana ngati munthu mmodzi ku
khwalala liri ku cipata ca kumadzi, namuuza Ezara mlembi atenge
buku la cilamulo ca Mose, cimene Yehova adalamulira
Israyeli. 2Ndipo Ezara wansembe anabwera naco cilamulo pamaso
pa msonkhano, ndiwo amuna ndi akazi, ndi yense wakumva ndi
kuzindikira tsiku loyamba la mwezi wacisanu ndi
ciwiri. 3Nawerenga m'menemo pa khwalala liri ku cipata ca
kumadzi kuyambira mbanda kuca kufikira msana, pamaso pa
amuna ndi akazi, ndi iwo okhoza kuzindikira; ndi anthu onse
anacherera khutu buku la cilamulo. 4Ndipo Ezara mlembi anaima
pa ciunda ca mitengo adacimangira msonkhanowo; ndi pambali:
pace padaima Matitiya, ndi Sema, ndi Anaya, ndi Uriya, ndi
Hilikiya, ndi Maaseya, ku dzanja lamanja lace; ndi ku dzanja
lamanzere Pedaya, ndi Misayeli, ndi Malikiya, ndi Hasumu, ndi
Hasibadana, Zekariya, ndi Mesulamu. 5Ndipo Ezara anafunyulula
bukulo pamaso pa anthu onse, popeza iye anasomphokera anthu
onse; ndipo polifunyulula anthu onse ananyamuka. 6Pamenepo
Ezara analemekeza Yehova Mulungu wamkuru. Nabvomereza
anthu onse, ndi kuti, Amen, Amen; nakweza manja ao, nawerama,
nalambira Yehova nkhope zao pansi. 7Ndi Yesuwa, ndi Bani, ndi
Serebiya, Yamini, Akubu, Sabetai, Hodayi, Maaseya, Kelita, Azariya,
Yozabadi, Hanani, Pelaya, ndi Alevi, anadziwitsa anthu cilamuloco;
ndi anthu anali ciriri pamalo pao, 8Nawerenga iwo m'buku
m'cilamulo ca Mulungu momveka, natanthauzira, nawazindikiritsa
cowerengedwaco. 9Ndipo Nehemiya, ndiye kazembe, ndi Ezara
wansembe mlembiyo, ndi Alevi ophunzitsa anthu, ananena ndi
anthu onse, Lero ndilo lopatulikira Yehova Mulungu wanu,
musamacita maliro, musamalira misozi. Popeza anthu onse analira
misozi pakumva mau a cilamulo. 10Nanena naonso, Mukani
mukadye zonona, mukamwe zozuna, nimumtumizire gawo lace iye
amene sanamkonze ratu kanthu; cifukwa lero ndilo lopatulikira
Ambuye wathu; ndipo musamacita cisoni; pakuti cimwemwe ca
Yehova ndico mphamvu yanu. 11Ndipo Alevi anatontholetsa anthu
onse, ndi kuti, Khalani muli cete; pakuti lero ndi lopatulika;
musamacita cisoni. 12Napita anthu onse kudya ndi kumwa, ndi
kutumiza magawo, ndi kusekerera kwakukuru; popeza anazindikira
mau amene adawafotokozera.

Madyerero a misasa

13Ndipo m'mawa mwace akuru a nyumba za makolo a anthu onse,
ansembe, ndi Alevi anasonkhana pamodzi kwa Ezara mlembi, kuti
atole nzeru za mau a cilamulo. 14Napeza munalembedwa
m'cilamulo kuti Yehova analamulira ndi Mose, kuti ana a Israyeli

azikhala m'misasa pa madyerero a mwezi wacisanu ndi ciwiri, 15ndi kuti azilalikira ndi kumveketsa m'midzi mwao monse ndi m'Yerusalemu, ndi kuti, Muziturukira kuphiri, ndi kutengako nthambi za azitona, ndi nthambi za mitengo yamafuta, ndi nthambi za mitengo yamcisu, ndi zinkhwamba za migwalangwa, ndi nthambi za mitengo zothonana, kumanga nazo misasa monga munalembedwa. 16Naturuka anthu, nakazitenga, nadzimangira misasa, yense pa tsindwi la nyumba yace, ndi m'mabwalo ao, ndi m'mabwalo a nyumba ya Mulungu, ndi pa khwalala la cipata ca kumadzi, ndi pa khwalala la cipata ca Efraimu. 17Ndi msonkhano wonse wa iwo oturuka m'ndende anamanga misasa, nakhala m'misasamo; pakuti ciyambire masiku a Yesuwa mwana wa Nuni kufikira tsiku lija ana a Israyeli sanatero. Ndipo panali cimwemwe cacikuru. 18Anawerenganso m'buku la cilamulo ca Mulungu tsiku ndi tsiku, kuyambira tsiku loyamba kufikira tsiku lotsiriza. Nacita madyerero masiku asanu ndi awiri; ndi tsiku lacisanu ndi citaru ndilo msonkhano woletsa, monga mwa malemba.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Msonkhano wa kusala ndi kupemphera

1Ndipo tsiku la makumi awiri mphambu anai la mwezi uno ana a
Israyeli anasonkhana ndi kusala, ndi kubvala ciguduli, ndipo anali
ndi pfumbi. 2Nadzipatula a mbumba ya Israyeli kwa alendo onse,
naimirira, naulula zocimwa zao, ndi mphulupulu za makolo
ao. 3Naimima poima pao, nawerenga m'buku la cilamulo ca Yehova
Mulungu wao limodzi la magawo anai a tsiku; ndi limodzi la
magawo anai anaulula, napembedza Yehova Mulungu
wao. 4Pamenepo anaimirira pa ciunda ca Alevi Yesuwa, ndi Bani,
Kadimiyeli, Sebaniya, Buni, Serebiya, Bani, ndi Kenani, napfuula
ndi mau akuru kwa Yehova Mulungu wao. 5Nati Alevi, Yesuwa, ndi
Kadimiyeli, Buni, Hasabineya, Serebiya, Hodiya, Sebaniya, ndi
Petatiya, Imiririani, lemekezani Yehova Mulungu wanu ku nthawi za
nthawi; ndipo lilemekezeke dzina lanu la ulemerero, lokuzika
loposa cilemekezo ndi ciyamiko conse. 6Inu ndinu Yehova,
nokhanu; mwalenga thambo, kumwambamwamba, ndi khamu lao
lonse, dziko lapansi, ndi zonse ziri pomwepo, nyanja ndi zonse ziri
m'mwemo, ndi Inu muzisunga zamoyo zonsezi, ndi khamu la
kumwamba lilambira Inu. 7Inu ndinu Yehova Mulungu amene
munasankha Abramu ndi kumturutsa m'Uri wa Akasidi, ndi
kumucha dzina lace Abrahamu; 8ndipo munampeza mtima wace
wokhulupirika pamaso panu, nimunapangana naye kumpatsa dziko
la Akanani, Ahiti, Aamori, ndi Aperizi, ndi Ayebusi, ndi Agirigasi,
kulipereka kwa mbumba zace; ndipo mwakwaniritsa mau anu,
popeza Inu ndinu wolungama. 9Ndipo munapenya msauko wa
makolo athu m'Aigupto, nimunamva kupfuula kwao ku Nyanja
Yofiira, 10nimunacitira zizindikilo ndi zodabwiza Farao ndi akapolo
ace onse, ndi anthu onse a m'dziko lace; popeza munadziwa kuti
anawacitira modzikuza; ndipo munadzibukitsira dzina monga lero
lino. 11Ndipo munagawanitsa nyanja pamaso pao, napita iwo
pakati pa nyanja pouma, ndipo munaponya mozama owalondola,
ngati mwala m'madzi olimba. 12Munawatsogoleranso usana ndi
mtambo woti njo, ndi moto tolo usiku, kuwaunikira m'njira
akayendamo. 13Munatsikiranso pa phiri la Sinai, nimunalankhula
nao mocokera m'Mwamba, ndipo munawapatsa maweruzo
oyenera, ndi cilamulo coona, malemba, ndi malamulo okoma; 14ndi
Sabata lanu lopatulika munawadziwitsa, nimunawalamulira
malamulo, ndi malemba, ndi cilamulo, mwa dzanja la Mose
mtumiki wanu; 15ndi mkate wocokera m'mwamba munawapatsa
pa njala yao; ndi madzi oturuka m'thanthwe munawaturutsira pa
ludzu lao, ndi kuwauza alowe, nalandire dziko limene
mudakwezapo dzanja lanu kuwapatsa. 16Koma iwo ndi makolo athu
anacita modzikuza, naumitsa khosi lao, osamvera malamulo

anu, 17nakana kumvera, osakumbukilansozodabwiza zanu munazicita pakati pao; koma anaumitsa khosi lao, ndipo m'kupanduka kwao anaika mtsogoleri abwerere kumka ku ukapolo wao; koma Inu ndinu Mulungu wokhululukira, wacisomo, ndi wansoni, wolekereza, ndi wocuruka cifundo; ndipo simunawasiya. 18Ngakhale apa atadzipangira mwana wa ng'ombe woyenga, nati, Suyu Mulungu wako anakukweza kucokera ku Aigupto, nacita zopeputsa zazikuru; 19koma Inu mwa nsoni zanu zazikuru simunawasiya m'cipululu; mtambo woti njo sunawacokera usana kuwatsogolera m'njira, ngakhale moto wa tolo usiku kuwaunikira panjira anayenera kuyendamo. 20Munawapatsanso mzimu wanu wokoma kuwalangiza, ndipo simunawamana mana anu pakamwa pao; munawapatsanso madzi pa ludzu lao. 21Ndipo munawalera zaka makumi anai m'cipululu, osasowa kanthu iwo; zobvala zao sizinatha, ndi mapazi ao sanatupa. 22Munawapatsanso maufumu, ndi mitundu ya anthu, nimunawagawa m'madera, motero analandira likhale lao lao dziko la Sihoni, ndilo dziko la mfumu ya ku Hesiboni, ndi dziko la Ogi mfumu ya ku Basana. 23Ana aonso munawacurukitsa monga nyenyezi za m'mwamba, nimunawalowetsa m'dziko mudalinena kwa makolo ao, alowemo likhale lao lao. 24Nalowa anawo, nalandira dzikoli likhale lao lao, ndipo munagonjetsa pamaso pao okhala m'dziko, ndiwo Akanani, ndi kuwapereka m'dzanja mwao, pamodzi ndi mafumu ao, ndi mitundu ya anthu ya m'dziko, kuti acite nao cifuniro cao. 25Ndipo analanda midzi yamalinga, ndi dziko la zonona, nalandira zikhale zao zao nyumba zodza la ndi zokoma ziri zonse, zitsime zokumbidwa, minda yampesa, ndi minda yaazitona, ndi mitengo yambiri yazipatso; nadya iwo, nakhuta, nanenepa, nakondwera nako kukoma kwanu kwakukuru. 26Koma anakhala osamvera, napandukira Inu, nataya cilamulo canu m'mbuyo mwao napha aneneri anu akuwacitira umboni, kuwabwezera kwa Inu, nacita zopeputsa zazikuru. 27Cifukwa cace munawapereka m'dzanja la adani ao akuwasautsa; koma mu nthawi ya kusautsika kwao anapfuula kwa Inu, ndipo munamva m'Mwamba, ndi monga mwa nsoni zanu zambiri munawapatsa apulumutsi akuwapulumutsa m'dzanja la adani ao. 28Koma atapumula, anabwereza kucita coipa pamaso panu; cifukwa cace munawasiya m'dzanja la adani ao amene anacita ufumu pa iwo; koma pobwera iwo ndi kupfuula kwa Inu, munamva m'Mwamba ndi kuwapulumutsa kawiri kawiri, monga mwa cifundo canu; 29ndipo munawacitira umboni, kuti muwabwezerenso ku cilamulo canu; koma anacita modzikuza, osamvera malamulo anu; koma anacimwira malamulo anu (amene munthu akawacita adzakhala nao ndi moyo); nakaniza phewa lao, naumitsa khosi lao,

osamvera. 30Koma munawalekerera zaka zambiri, ndi kuwacitira
umboni ndi mzimu wanu, mwa aneneri anu, koma sanamvera;
cifukwa cace munawapereka m'dzanja la mitundu ya anthu a
m'dziko. 31Ndipo mwa nsoni zanu zocuruka simunawatha, kapena
kuwataya; popeza Inu ndinu Mulungu wa cisomo ndi
cifundo. 32Ndipo tsono, Mulungu wathu, ndinu Mulungu wamkuru,
ndi wamphamvu, ndi woopsa, wakusunga pangano ndi cifundo,
asacepe pamaso panu mabvuto athu onse amene anatigwera ife,
ndi mafumu athu, akuru athu, ndi ansembe athu, ndi aneneri athu,
ndi makolo athu, ndi anthu anu onse, kuyambira masiku a mafumu
a Asuri, mpaka lero lino. 33Koma Inu ndinu wolungama mwa zonse
zatigwera; pakuti mwacita zoona, koma ife tacita coipa; 34ndi
mafumu athu, akuru athu, ansembe athu, ndi makolo athu,
sanasunga cilamulo canu, kapena kumvera malamulo anu, ndi
mboni zanu, zimene munawacitira umboni nazo. 35Popeza
sanatumikira Inu m'ufumu wao, ndi m'ubwino wanu wocuruka
umene mudawapatsa, ndi m'dziko lalikuru ndi la zonona
mudalipereka pamaso pao, ndipo sanabwerera kuleka nchito zao
zoipa. 36Tapenyani, ife lero ndife akapolo, ndi dzikoli mudalipereka
kwa makolo athu kudya zipatso zace ndi zokoma zace, taonani, ife
ndife akapolo m'menemo. 37Ndipo licurukitsira mafumu zipatso
zace, ndiwo amene munawaika atiweruze, cifukwa ca zoipa zathu;
acitanso ufumu pa matupi athu, ndi pa zaweta zathu, monga umo
akonda; ndipo ife tisauka kwakukuru. 38Ndipo mwa ici conse ticita
pangano lokhazikika, ndi kulilemba, ndi akulu athu, Alevi athu, ndi
ansembe athu, alikomera cizindikilo.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Pangano lokhazikika pakati pa anthu ndi Mulungu

1Okomera cizindikilo tsono ndiwo Nehemiya, Tirisata mwana wa
Hakaliya, ndi Zedekiya, 2Seraya, Agariya, Yeremiya, 3Pasuri,
Amariya, Malikiya, 4Hatusi, Sebaniya, Maluki, 5Harimu, Meremoti,
Obadiya, 6Danieli, Ginetoni, Baruki, 7Mesulamu, Abiya,
Miyamini, 8Maaziya, Biligai, Semaya, ndiwo ansembe. 9Ndi Alevi
ndiwo Yesuwa mwana wa Azaniya, Binui wa ana a Henadadi,
Kadiniyeli; 10ndi abale ao: Sebaniya, Hodiya, Kelita, Pelaya,
Hanani, 11Mika, Rehobo, Hasabiya, 12Zakuri, Serebiya,
Sebaniya, 13Hodiya, Bani, Beninu. 14Akuru a anthu: Parosi, Patati,
Moabu, Elamu, Zatu, Bani, 15Buni, Azigadi, Bebai, 16Adoniya,
Bigivai, Adini, 17Ateri, Hezekiya, Azuri, 18Hodiya, Hasumu,
Bezai, 19Harifi, Anatoti, Nobai, 20Magipiasi, Mesulamu,
Heziri, 21Mesezabele, Zadoki, Yaduwa, 22Pelatiya, Hanani,
Ananiya, 23Hoseya, Hananiya, Hasubi, 24Halohesi, Pila,
Sobeki, 25Rehumu, Hasabina, Maaseya, 26ndi Ahiya, Hanani,
Anani, 27Maluki, Harimu, Baana. 28Ndi anthu otsala, ansembe,
Alevi, odikira, oyimbira, Anetini, ndi onse anadzisiyanitsawo pa
mitundu ya anthu a m'dziko kutsata cilamulo ca Mulugu, akazi ao,
ana ao amuna ndi akazi, yense wodziwa ndi
wozindikira, 29amenewa anaumirira abale ao, omveka ao, nalowa
m'temberero ndi lumbiro, kuti adzayenda m'cilamulo ca Mulungu
anacipereka Mose mtumiki wa Mulungu, ndi kuti adzasunga ndi
kucita zonse atilamulira Yehova Ambuye wathu, ndi maweruzo ace,
ndi malemba ace; 30ndi kuti sitidzapereka ana athu akazi kwa
mitundu ya anthu a m'dziko, kapena kutengera ana athu amuna
ana ao akazi; 31ndipo mitundu ya anthu a m'dziko akabwera nao
malonda, ngakhale tirigu, dzuwa la Sabata, kutsata malonda,
sitidzagulana nao dzuwa la Sabata, kapena dzuwa lina lopatulika,
ndi kuti tidzaleka caka cacisanu ndi ciwiri ndi mangawa ali
onse. 32Tinadziikiranso malamulo, kuti tizipereka caka ndi caka
limodzi la magawo atatu a sekeli ku nchito ya nyumba ya Mulungu
wathu; 33kuliperekera mkate woonekera, ndi nsembe yaufa
yosaleka, ndi nsembe yopsereza yosaleka, ya masabata, ya
pokhala miyezi, kuliperekera nyengo zoikika ndi zopatulikira, ndi
nsembe za zolakwa za kutetezera Israyeli zoipa, ndi nchito zonse
za nyumba ya Mulungu wathu. 34Ndipo tinalota maere, ansembe,
Alevi, ndi anthu, a copereka ca nkhuni, kubwera nazo ku nyumba
ya Mulungu wathu, monga mwa nyumba za makolo athu, pa
nyengo zoikika caka ndi caka, kuzisonkha pa guwa la nsembe la
Yehova Mulungu wathu, monga mulembedwa m'cilamulo; 35ndi
kubwera nazo zipatso zoyamba za nthaka, ndi zoyamba za zipatso
zonse za mtengo uli wonse caka ndi caka, ku nyumba ya

Yehova; 36ndi ana athu oyamba kubadwa, ndi oyamba kubadwa a nyama zathu, monga mulembedwa m'cilamulo, ndi oyamba a ng'ombe zathu, ndi nkhosa zathu, kubwera nazo ku nyumba ya Mulungu wathu kwa ansembe akutumikira m'nyumba ya Mulungu wathu; 37ndi kuti tidzabwera nazo za mtanda wa mkate wathu woyamba, ndi nsembe zathu zokwera, ndi zipatso za mtengo uli wonse, vinyo, ndi mafuta, kwa ansembe, ku zipinda za nyumba ya Mulungu wathu; ndi limodzi la magawo khumi la nthaka yathu kwa Alevi; pakuti Alevi amene amalandira limodzi limodzi la magawo khumi m'midzi yonse yolima ife. 38Ndipo wansembe mwana wa Aroni azikhala ndi Alevi, polandira Alevi limodzi limodzi la magawo khumi; ndi Alevi azikwera nalo limodzi la magawo khumi mwa limodzi limodzi la magawo khumi ku nyumba ya Mulungu wathu, kuzipinda, ku nyumba ya cuma. 39Pakuti ana a Israyeli ndi ana a Levi, azibwera nayo nsembe yokweza yatirigu, ndi yavinyo ndi yamafuta, kuzipinda kuli zipangizo za malo opatulika, ndi ansembe akutumikira, ndi odikira, ndi oyimbira; kuti tisasiye nyumba ya Mulungu wathu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Ena akhala m'Yerusalemu, ena m'midzi yina

1Ndipo akuru anthu anakhala m'Yerusalemu; anthu otsala omwe
anacita maere, kuti libwere limodzi la magawo khumi likhale
m'Yerusalemu, mudzi wopatulika, ndi asanu ndi anai a khumi
m'midzi yina. 2Ndipo anthu anadalitsa amuna onse a akudzinenera
mwaufulu kuti adzakhala m'Yerusalemu.
3Awa tsono ndi akulu a dziko okhala m'Yerusalemu; koma m'midzi
ya Yuda yense anakhala pa colowa cace m'midzi mwao, ndiwo
Israyeli, ansembe, ndi Alevi, ndi Anetini, ndi ana a akapolo a
Solomo. 4Ndipo m'Yerusalemu munakhala ena a ana a Yuda ndi a
ana a Benjamini. Mwa ana a Yuda: Ataya mwana wa Uziya, mwana
wa Zekariya, mwana wa Amariya, mwana wa Sefatiya, mwana wa
Mahalaleli, wa ana a Perezi; 5ndi Maaseya mwana wa Baruki,
mwana wa Koloze, mwana wa Huzaya, mwana wa Adaya, mwana
wa Yoyaribi, mwana wa Zekariya, mwana wa Msiloni. 6Ana onse a
Perezi okhala m'Yerusalemu ndiwo ngwazi mazana anai mphambu
makumi asanu ndi limodzi kudza asanu ndi atatu. 7Ndi ana a
Benjamini ndi awa: Salu mwana wa Mesulamu, mwana wa Yoedi,
mwana wa Pedaya, mwana Wa Kolaya, mwana wa Maseya, mwana
wa Itiyeli, mwana wa Yesaya. 8Ndi wotsatananaye Gabai, Salai,
mazana asanu ndi anai mphambu makumi awiri kudza asanu ndi
atatu. 9Ndi Yoeli mwana wa Zikiri ndiye woyang'anira wao, ndi
Yuda mwana wa Hasenuwa ndiye wothandizana naye,
poyang'anira mudzi. 10Mwa ansembe: Yedaya mwana wa Yoyaribi,
Yakini, 11Seraya mwana wa Hilikiya, mwana wa Mesulamu, mwana
wa Zadoki, mwana wa Merayoti, mwana wa Ahitubu mtsogoleri wa
m'nyumba ya Mulungu; 12ndi abale ao ocita nchito ya m'nyumbayi
ndiwo mazana asanu ndi atatu mphambu makumi awiri kudza
awiri; ndi Adaya mwana wa Yerohamu, mwana wa Pelaliya, mwana
wa Amzi, mwana wa Zekariya, mwana: wa Pasuru, mwana wa
Malikiya; 13ndi abale ace akulu a nyumba za makolo awiri
mphambu makumi anai kudza awiri, ndi Amasai mwana wa Azareli,
mwana wa Azai, mwana wa Mesilimoti, mwana wa Imeri; 14ndi
abale ao, ngwazi zamphamvu, zana limodzi mphambu makumi
awiri kudza asanu ndi atatu; ndi woyang'anira wao ndiye Zabidiyeli
mwana wa Hagedolimu. 15Ndi mwa Alevi: Semaya mwana wa
Hasubu, mwana wa Azirikamu, mwana wa Hasabiya, mwana wa
Buni; 16ndi Sabetai, ndi Yozabadi, mwa akuru a Alevi,
anayang'anira nchito za pabwalo za nyumba ya Mulungu; 17ndi
Mataniya mwana wa Mika, mwana wa Zabidi, mwana wa Asafu,
ndiye mkuru wakuyamba mayamiko, popemphera; ndi Bakibukiya
wotsatana naye mwa abale ace, ndi Abida mwana wa Samua,
mwana wa Galali, mwana wa Yedutuni. 18Alevi onse m'mudzi

wopatulikawo ndiwo mazana awiri mphambu makumi asanu ndi atatu kudza anai. 19Ndi odikira: Akubu, Talimoni, ndi abale ao akulindira pazipata, ndiwo zana limodzi mphambu makumi asanu ndi awiri kudza awiri. 20Ndi Aisrayeli otsala, ndiwo ansembe ndi Alevi, anakhala m'midzi yonse ya Yuda, yense m'colowa cace. 21Koma Anetini anakhala m'Ofeli, ndi Ziya, ndi Gisipa anali oyang'anira Anetini. 22Ndipo woyang'anira wa Alevi m'Yerusalemu ndiye Uzi mwana wa Bani, mwana wa Hasabiya, mwana wa Mataniya, mwana wa Mika; mwa ana a Asafu oyimbira ena anayang'anira nchito ya m'nyumba ya Mulungu. 23Pakuti mfumu inalamulira za iwowa, naikira oyimbira cowathandiza, yense cace pa tsiku lace. 24Ndi Petatiya mwana wa Mesezabele, wa ana a Zera, mwana wa Yuda, anatumikira mfumu pa mirandu yonse ya anthuwo. 25Ndi ana ena a Yuda anakhala m'midzi ya ku minda yao, m'Kiriyati Ariba ndi miraga yace, ndi m'Diboni ndi miraga yace, ndi m'Yekabizeeli ndi midzi yace, 26ndi m'Yesuwa, ndi m'Molada, ndi Betepeleti, 27ndi m'Hazarisuala, ndi m'Beereseba ndi miraga yace, 28ndi m'Zikilaga, ndi m'Mekona ndi miraga yace, 29ndi m'Enirimoni, ndi m'Zora, ndi m'Yarimuti, 30Zanowa, Adulamu ndi midzi yao, Lakisi ndi minda yace, Azeka ndi miraga yace. Ndipo anamanga misasa kuyambira ku Beereseba mpaka cigwa ca Hinomu. 31Ana a Benjamini omwe, kuyambira ku Geba pa Mikimasi, ndi Aiya, ndi pa Beteli ndi miraga yace, 32pa Anatoti, Nobi, Ananiya, 33Hazori, Rama, Gitaimu, 34Hadidi, Zeboimu, Nebalati, 35Lodi, ndi Ono, cigwa ca amisiri. 36Ndi magawo a Levi anakhala ena ku Yuda, ndi ena ku Benjamini.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Maina a ansembe ndi Alevi ofika ku Yerusalemu pamodzi ndi Zerubabele

1Ndipo ansembe ndi Alevi amene anakwera ndi Zerubabele mwana
wa Sealtiyeli, ndi Yesuwa, ndi awa: Seraya, Yeremiya,
Ezara, 2Amariya, Maluki, Hatusi, 3Sekaniya, Rehumu,
Meremoti, 4Ido, Ginetoi, Abiya, 5Miyamini, Maadiya,
Biliga, 6Semaya, ndi Yoyaribi, Yedaya, 7Salu, Amoki, Hilikiya,
Yedaya. Awa ndi akuru a ansembe ndi abale ao m'masiku a
Yesuwa. 8Ndi Alevi ndiwo Yesuwa, Binui, Kadimiyeli, Serebiya, Yuda,
ndi Mataniya; iye ndi abale ace amatsogolera mayamiko. 9Ndi
Bakibukiya ndi Uni, abale ao, anawayang'anira maulonda. 10Ndi
Yesuwa anabala Yoyakimu, ndi Yoyakimu anabala Eliasibi ndi
Eliasibi anabala Yoyada, 11ndi Yoyada anabala Yonatani, ndi
Yonatani, anabala Yaduwa. 12Ndi m'masiku a Yoyakimu ansembe
akulu a nyumba za makolo ndiwo: wa Seraya, Meraya; wa
Yeremiya, Hananiya; 13wa Ezara, Mesulamu; wa Amariya,
Yehohanana; 14wa Maluki, Yonatani; wa Sebaniya, Yosefe; 15wa
Harimu, Adina; wa Merayoti, Helikai; 16wa Ido, Zekariya; wa
Ginetoni, Mesulamu; 17wa Abiya, Zikiri; wa Minyamini, wa Moadiya,
Pilitai; 18wa Biliga, Samura; wa Semaya, Yehonatani; 19ndi wa
Yoyaribi, Matani; wa Yedaya, Uzi; 20wa Salai, Kalai; wa Amoki,
Eberi; 21wa Hilikiya, Hasabiya; wa Yedaya, Netaneli. 22M'masiku a
Ehasibi, Yoyada, Yohanana, ndi Yoduwa, Alevi analembedwa akuru
a nyumba za makolo; ansembe omwe, mpaka ufumu wa Dariyo wa
ku Perisiya. 23Ana a Levi, akuru a nyumba za makolo,
analembedwa m'buku la macitidwe, mpaka masiku a Yohanana
mwana wa Eliasibu. 24Ndi akuru a Alevi: Hasabiya, Serebiya, ndi
Yesuwa mwana wa Kadimiyeli, ndi abale ao openyana nao,
kulemekeza ndi kuyamika, monga mwa lamulo la Davide munthu
wa Mulungu, alonda kupenyana alonda. 25Mataniya, ndi
Bakibukiya, Obadiya, Mesulamu, Talimoni, Akubi, ndiwo odikira
akulonda pa nyumba za cuma ziri kuzipata. 26Awa anakhala
m'masiku a Yoyakimu mwana wa Yesuwa, mwana wa Yozadaki, ndi
m'masiku a Nehemiya kazembe, ndi a Ezara wansembe mlembiyo.

Kuperekedwa kwa linga la Yerusalemu

27Ndipo popereka linga la Yerusalemu anafunafuna Alevi m'malo
mwao monse, kubwera nao ku Yerusalemu, kuti acite kuperekaku
mokondwera, ndi mayamiko, ndi kuyimbira, ndi nsanje, zisakasa,
ndi azeze. 28Ana a oyimbirawo anasonkhana ocokera ku dziko
lozungulira Yerusalemu, ndi ku midzi ya Anetofati, 29ndi ku
Betegiligala, ndi ku minda ya Geba ndi Azimaveti; popeza
oyimbirawo adadzimangira midzi pozungulira Yerusalemu. 30Ndipo
ansembe ndi Alevi anadziyeretsa okha, nayeretsa anthu, ndi

zipata, ndi linga. 31Pamenepo ndinakwera nao akuru a Yuda pa
lingali, ndinaikanso oyamikira magulu awiri akuru oyenda
molongosoka; lina loyenda ku dzanja lamanja palinga kumka ku
cipata ca kudzala; 32ndi pambuyo pao anayenda Hosaya, ndi
limodzi la magawo awiri a akuru a Yuda, 33ndi Azariya, Ezara ndi
Mesulamu, 34Yuda, ndi Benjamini, ndi Semaya, ndi Yeremiya, 35ndi
ana ena a ansembe ndi malipenga: Zekariya mwana wa Yonatani,
mwana wa Semaya, mwana wa Mataniya, mwana wa Mikaya,
mwana wa Zakuri, mwana wa Asafu, 36ndi abale ace: Semaya, ndi
Azareli, Milalai, Gilelai, Maai, Netaneli, ndi Yuda, Hanani, ndi
zoyimbira za Davide munthu wa Mulungu; ndi Ezara mlembiyo
anawatsogolera; 37ndi ku cipata ca kucitsime, ndi kundunji kwao,
anakwerera pa makwerero a mudzi wa Davide, potundumuka
linga, popitirira pa nyumba ya Davide, mpaka ku cipata ca kumadzi
kum'mawa. 38Ndi gulu lina la oyamikira linamuka mokomana nao,
ndi ine ndinawatsata, pamodzi ndi limodzi la magawo awiri la
anthu palinga, napitirira pa nsanja ya ng'anjo, mpaka ku linga
lacitando; 39ndi pamwamba pa cipata ca Efraimu, ndi ku cipata
cakale, ndi ku cipata cansomba, ndi nsanja ya Hananeli, ndi nsanja
ya Hameya, mpaka ku cipata cankhosa; ndipo anaima ku cipata
cakaidi. 40Atatero, magulu awiriwo a iwo oyamikira anaima
m'nyumba ya Mulungu, ndipo ine ndi limodzi la magawo awiri a
olamulira pamodzi ndi ine; 41ndi ansembe, Eliakimu, Maaseya,
Minyamini, Mikaya, Elioenai, Zekariya, ndi Hananiya, ali nao
malipenga; 42ndi Maaseya, ndi Semaya, ndi Eleazara, ndi Uzi, ndi
Yehohanana, ndi Malikiya, ndi Elamu, ndi Ezeri. Ndipo oyimbira
anayimbitsa Yeziraya ndiye woyang'anira wao. 43Ndipo anaphera
nsembe zambiri tsiku lija, nasekerera; pakuti Mulungu
anawakondweretsa ndi cimwemwe cacikuru; ndi akazi omwe ndi
ana anakondwera; ndi cikondwerero ca Yerusalemu cinamveka
kutali.

Akonzanso za kupereka limodzi la magawo khumi

44Ndipo tsiku lomwelo anaika anthu asunge zipinda za cuma, za
nsembe zokweza, za zipatso zoyamba, ndi za limodzi limodzi la
magawo khumi, kulonga m'mwemo, monga mwa minda ya midzi,
magawo onenedwa ndi cilamulo, akhale a ansembe ndi Alevi;
popeza Yuda anakondwera nao ansembe ndi Alevi
lakuimirirako. 45Ndipo iwo anasunga udikiro wa Mulungu wao, ndi
udikiro wa mayeretsedwe; momwemonso oyimbira ndi odikira,
monga mwa lamulo la Davide ndi la Solomo mwana wace. 46Pakuti
m'masiku a Davide ndi Asafu kalelo kunali mkuru wa oyimbira, ndi
wa nyimbo zolemekeza ndi zoyamikira Mulungu. 47Ndi Aisrayeli
onse m'masiku a Zerubabele, ndi m'masiku a Nehemiya,
anapereka magawo a oyimbira ndi odikira, monga mudafunika

tsiku ndi tsiku; nawapatulira Alevi; ndi Alevi anawapatulira ana a Aroni.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Tobiya acotsedwa ku Kacisi

1Tsiku lomwelo anawerenga m'buku la Mose m'makutu a anthu,
napeza m'menemo kuti Aamoni ndi Amoabu asalowe mu
msonkhano wa Mulungu ku nthawi yonse; 2popeza
sanawacingamira ana a Israyeli ndi cakudya ndi madzi, koma
anawalemberera Balamu awatemberere; koma Mulungu wathu
anasanduliza tembererolo likhale mdalitso. 3Ndipo kunali, atamva
cilamuloco, anasiyanitsa pa Israyeli anthu osokonezeka onse.
4Cinkana ici, Eliasibu wansembe, woikidwa asunge zipinda za
nyumba ya Mulungu wathu, anacita cibale ndi
Tobiya, 5namkonzera cipinda cacikuru, kumene adasungira kale
zopereka za ufa, libano, ndi zipangizo, ndi limodzi limodzi la
magawo khumi a tirigu, vinyo, ndi mafuta, zolamutidwira Alevi, ndi
oyimbira, ndi odikira, ndi nsembe zokweza za ansembe. 6Koma
pocitika ici conse sindinakhala ku Yerusalemu; pakuti caka ca
makumi atatu ndi caciwiri ca Aritasasta mfumu ya Babulo ndinafika
kwa mfumu, ndipo atapita masiku ena ndinapempha mfumu
indilole; 7ndipo ndinafika ku Yerusalemu, ndi kuzindikira coipa
anacicita Eliasibu, cifukwa ca Tobiya, ndi kumkonzera cipinda
m'mabwalo a nyumba ya Mulungu. 8Ndipo ndinaipidwa naco
kwambiri, motero ndinataya kubwalo akatundu onse a m'nyumba
ya Tobiya, kuwacotsa m'cipindamo. 9Pamenepo ndinalamulira,
ndipo anayeretsa zipindazo; ndipo ndinabwezeramonso zipangizo
za nyumba ya Mulungu, pamodzi ndi zopereka za ufa ndi
libano. 10Ndinazindikiranso kuti sanapereka kwa Alevi magawo ao;
m'mwemo Alevi ndi oyimbira adathawira yense ku munda
wace. 11Potero ndinatsutsana nao olamulira, ndinati, Yasiyidwiranji
nyumba ya Mulungu? Ndipo ndinawasonkhanitsa, ndi kuwafka
m'malo mwao. 12Ndi Ayuda onse anabwera nalo limodzi limodzi la
magawo khumi a tirigu, ndi vinyo, ndi mafuta, ku nyumba za
cuma. 13Ndinaikanso osunga cuma, asunge nyumba za cuma:
Selemiya wansembe, ndi Zadoki mlembi; ndi wa Alevi, Pedaya; ndi
wakuwathandiza, Hanani mwana wa Zakuri, mwana wa Mataniya;
popeza anayesedwa okhulupirika ndi udindo wao, ndiwo kugawira
abale ao. 14Mundikumbukile Mulungu wanga mwa ici,
nimusafafanize zokoma zanga ndinazicitira nyumba ya Mulungu
wanga, ndi maudikiro ace.

D'zuwa la Sabata likhalanso lopatulika

15Masiku awa ndinaona ku Yuda ena akuponda mphesa
m'coponderamo dzuwa la Sabata, ndi akubwera nayo mitolo ya
tirigu, ndi kuisenzetsa pa aburu; momwemonso vinyo, mphesa, ndi
nkhuyu, ndi zosenza ziri zonse, zimene analowa nazo
m'Yerusalemu dzuwa la Sabata, ndipo ndinawacitira umboni

wakuwatsutsa tsikuti anagulitsa zakudya. 16Anakhalanso
m'menemo a ku Turo, obwera nazo nsomba, ndi malonda ali onse,
nagulitsa dzuwa la Sabata kwa ana a Yuda ndi
m'Yerusalemu. 17Pamenepo ndinatsutsana nao aufulu a Yuda,
ndinanena nao, Cinthu canji coipa ici mucicita, ndi kuipsa naco
dzuwa la Sabata? 18Sanatero kodi makolo anu, ndipo Mulungu
wathu anatifikitsira ife ndi mudzi uno coipa ici conse? koma inu
muonjezera Israyeli mkwiyo pakuipsa Sabata. 19Ndipo kunali,
kukadayamba cizirezire pa zipata za Yerusalemu, losafika Sabata,
ndinawauza atseke pamakomo; ndinawauzanso kuti asatsegulepo,
koma litapita Sabata ndipo; ndipo ndinaimika anyamata anga ena
pazipata, kuti pasalowe katundu dzuwa la Sabata. 20Momwemo eni
malonda ndi ogulitsa malonda ali onse, anagona kunja kwa
Yerusalemu kamodzi kapena kawiri. 21Koma ndinawacima umboni
wakuwatsutsa, ndinanena nao, Mugoneranji pafupi pa linga?
mukateronso ndikuthirani manja. Kuyambira pomwepo sanafikanso
pa Sabata. 22Ndipo ndinauza Alevi kuti adziyeretse, nabwere,
nasunge pazipata kupatula dzuwa la Sabata. Mundikumbukire
Icinso, Mulungu wanga, ndi kundileka monga mwa cifundo canu
cacikuru.

Nehemiya awadzudzula pa kukwatira akazi akunja

23Masiku aja ndinaonanso Ayudawo anadzitengera akazi a Asidodi,
Aamoni, ndi Amoabu, 24ndi ana ao analankhula mwina Ciasidodi,
osadziwitsa kulankhula Ciyuda, koma monga umo amalankhula
mtundu wao uli wonse. 25Ndipo ndinatsutsana nao, ndi
kuwatemberera, ndi kukantha ena a iwo, ndi kumwetula tsitsi lao,
ndi kuwalumbiritsa pa Mulungu ndi kuti, Musapereka ana anu akazi
kwa ana ao amuna, kapena kutengera ana anu amuna, kapena a
inu nokha, ana ao akazi. 26Nanga Solomo mfumu ya Israyeli
sanacimwa nazo zinthu izi? cinkana mwa amitundu ambiri panalibe
mfumu ngati iye, ndi Mulungu wace anamkonda, ndi Mulungu wace
anamlonga mfumu ya Aisrayeli onse; koma ngakhale iye, akazi
acilendo anamcimwitsa. 27Ndipo kodi tidzamvera inu, kucita coipa
ici cacikuru conse, kulakwira Mulungu wathu ndi kudzitengera
akazi acilendo? 28Koma wina wa ana a Yoyada, mwana wa Eliasibu
mkuru wa ansembe, anali mkamwini wa Sanibalati Mhoroni;
cifukwa cace ndinampitikitsa kumcotsa kwa ine. 29Muwakumbukile
Mulungu wanga, popeza anadetsa unsembe, ndi pangano la
unsembe, ndi la Alevi. 30Momwemo ndinawayeretsa kuwacotsera
acilendo onse, ndi kuikira udikiro ansembe ndi Alevi, yense ku
nchito yace; 31ndi copereka ca nkhuni pa nthawi zoikika, ndi wa
zipatso zoyamba. Mundikumbukile, Mulungu wanga, cindikomere.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Esther

Estere 1

Madyerero a Ahaswero

1IZI zinacitika masiku a Ahaswero, ndiye Ahasweroyo anacita
ufumu kuyambira Indiya kufikira Kusi, pa maiko zana limodzi
mphambu makumi awiri kudza asanu ndi awiri. 2Masiku ajawo,
pokhala Ahaswero pa mpando wa ufumu wace uli m'cinyumba ca
ku Susani, 3caka cacitatu ca ufumu wace, anakonzera madyerero
akalonga ace onse, ndi omtumikira; amphamvu a Perisiya ndi
Mediya, omveka ndi akalonga a maikowo anakhala pamaso
pace, 4pamene anaonetsa zolemera za ufumu wace waulemu, ndi
ulemerero wa ukulu wace woposa, masiku ambiri, ndiwo masiku
zana limodzi, mphambu makumi asanu ndi atatu. 5Atatha
masikuwa, mfumu inakonzera madyerero anthu onse okhala
m'cinyumba ca ku Susani, akulu ndi ang'ono, masiku asanu ndi
awiri, ku bwalo la munda wa maluwa wa ku cinyumba ca
mfumu; 6panali nsaru zolenjeka zoyera, zabiriwiri, ndi zamadzi,
zomangika ndi zingwe za thonje labafuta, ndi lofiirira, pa zigwinjiri
zasiliva, ndi nsanamira zansangalabwi; makama anali a golidi ndi
siliva pa mayalidwe a miyala yofiira, ndi yoyera, ndi yoyezuka, ndi
yakuda. 7Nawapatsa cakumwa m'zomwera zagolidi, zomwerazo
nzosiyana-siyana, ndi vinyo wacifumu anacuruka, monga mwa
ufulu wa mfumu. 8Ndi mamwedwewo anali monga mwa lamulo;
panalibe kukakamiza; pakuti mfumu idaikira akulu onse a nyumba
yace motero, kuti acite monga momwe akhumba ali yense.

Vasiti akana kuoneka kumadyerero

9Vasiti yemwe, mkazi wamkuru, anakonzera akazi madyerero
m'nyumba yacifumu ya mfumu Ahaswero. 10Tsiku lacisanu ndi
ciwiri, pokondwera mtima wa mfumu ndi vinyo, iye anauza
Mehumani, Bizita, Haribona, Bigita, ndi Abagita, Zetara, ndi
Karikasi, adindo asanu ndi awiriwo akutumikira pamaso pa mfumu
Ahaswero, 11abwere naye Vasiti mkazi wamkuru pamaso pa
mfumu ndi korona wacifumu, kuonetsa anthu ndi akuru kukoma
kwace; popeza anali wokongola maonekedwe ace. 12Koma Vasiti
mkazi wamkuruyo anakana kudza pa mau a mfumu adamuuza
adindowo; potero mfumu idapsa mtima ndithu, ndi mkwiyo wace
unatentha m'kati mwace.

Vasiti acotsedwa

13Pamenepo mfumu inanena kwa eni nzeru, akudziwa za
m'tsogolo, mfumu idafotero nao onse akudziwa malamulo ndi
maweruzo, 14a pafupi naye ndiwo Karisena. Setara, Adimata,
Tarisisi, Meresi, Marisena, ndi Memukana, akalonga asanu ndi awiri
a Perisiya ndi Mediya, openya nkhope ya mfumu ndi kukhala

oyamba m'ufumu. 15Anati, Tidzacitanji naye mkazi wamkuru Vasiti
monga mwa malamulo, popeza sanacita comuuza mfumu
Ahaswero mwa adindo? 16Ndi Memukana anati pamaso pa mfumu
ndi akalonga, Vasiti mkazi wamkuru sanalakwira mfumu yekha,
komanso akalonga onse, ndi mitundu yonse ya anthu okhala
m'maiko onse a mfumu Ahaswero. 17Pakuti macitidwe awa a mkazi
wamkuruyo adzabuka kufikira akazi onse, kupeputsa amuna ao
pamaso pao; anthu akati, Mfumu Ahaswero anati abwere naye
Vasiti mkazi wamkuru pamaso pace, koma sanadza iye. 18Inde
tsiku lomwelo akazi akuru a Perisiya ndi Mediya, atamva macitidwe
a mkazi wamkuruyo, adzatero nao momwemo kwa akalonga onse
a mfumu. Ndi cipeputso ndi mkwiyo zidzacuruka. 19Cikakomera
mfumu, aturuke mau acifumu pakamwa pace, nalembedwe
m'malamulo a Aperisiya ndi Amediya, angasinthike, kuti Vasiti
asalowenso pamaso pa mfumu Ahaswero; ndi mfumu aninkhe
cifumu cace kwa mnzace womposa iye. 20Ndipo mau amene
adzaika mfumu akamveka m'ufumu wace wonse, (pakuti ndiwo
waukuru), akazi onse adzacitira amuna ao ulemu, akulu ndi
ang'ono. 21Ndipo mauwo anakonda mfumu ndi akalonga; ndi
mfumu inacita monga mwa mau a Memukana, 22natumiza akalata
ku maiko onse a mfumu, ku dziko liri lonse monga mwa
cilembedwe cao, ndi ku mtundu uli wonse monga mwa cinenedwe
cao, kuti mwamuna ali yense akhale wamkuru m'nyumba yace
yace, nawabukitse monga mwa cinenedwe ca anthu amtundu
wace.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Ahaswero akwatira Estere

1Zitatha izi, utaleka mkwiyo wa mfumu Ahaswero, anakumbukila
Vasiti, ndi cocita iye, ndi comlamulidwira. 2Pamenepo anyamata a
mfumu omtumikira anati, Amfunire mfumu anamwali
okongola; 3ndi mfumu aike oyang'anira m'maiko onse a ufumu
wace, kuti asonkhanitse anamwali onse okongola m'cinyumba ca
ku Susani, m'nyumba ya akazi; awasunge Hege mdindo wa mfumu
wosungira akazi, nawapatse zowayeretsa; 4ndi namwali womkonda
mfumu akhale mkazi wamkuru m'malo mwa Vasiti. Ndipo cinthuci
cinamkonda mfumu, nacita comweco.
5Panali Myuda m'cinyumba ca ku Susani, dzina lace ndiye
Moredekai, mwana wa Yairi, mwana wa Simei, mwana wa Kisi
Mbenjamini; 6uyu anatengedwa ndende ku Yerusalemu, pamodzi
ndi andende anatengedwa pamodzi ndi Yekoniya mfumu ya Yuda,
amene Nebukadinezara mfumu ya Babulo adamtenga
ndende. 7Ndipo iye adalera Hadasa, ndiye Estere, mwana wamkazi
wa atate wace wamng'ono; popeza iye analibe atate kapena amai;
ndi namwaliyo anali wa maonekedwe okoma, ndi wokongola; ndipo
atamwalira atate wace ndi mai wace, Moredekai anamtenga
akhale mwana wace. 8Ndipo kunali, atamveka mau a mfumu ndi
lamulo lace, ndipo atasonkhanidwa anamwali ambiri m'cinyumba
ca ku Susani, awasunge Hege, anamtenga Estere yemwe, alowe
m'nyumba ya mfumu, amsunge Hege wosunga akazi. 9Ndipo
namwaliyo anamkomera, namcitira cifundo; ndipo anafulumira
kumpatsa zace zomyeretsa, ndi magawo ace, ndi anamwali asanu
ndi awiri oyenera kumpatsa ocokera m'nyumba ya mfumu; ndipo
anamsuntha iye ndi anamwali ace akhale m'malo okometsetsa
m'nyumba ya akazi. 10Estere sadaulula mtundu wace ndi cibale
cace; pakuti Moredekai adamuuzitsa kuti asadziulule. 11Ndi
Moredekai akayendayenda tsiku ndi tsiku ku bwalo la nyumba ya
akazi, kuti adziwe umo akhalira Estere, ndi cimene
cidzamcitikira. 12Kunafika tsono kulowa kwace kwa namwali ali
yense, kuti alowe kwa mfumu Ahaswero, atamcitira monga mwa
lamulo la akazi, miyezi khumi ndi iwiri; pakuti adafokwaniritsa
masiku a mayeretsedwe ao motero, miyezi isanu ndi umodzi ndi
mafuta a mure, ndi miyezi isanu ndi umodzi ndi zonunkhira bwino,
ndi zoyeretsa akazi. 13Ndipo namwali ali yense analowa kwa
mfumu matero, ziri zonse anafuna anampatsa zocokera m'nyumba
ya akazi, alowe nazo ku nyumba ya mfumu. 14Madzulo ace
analowamo, nabwera m'mawa mwace kumka ku nyumba yaciwiri
ya akazi, amsunge Saasigazi mdindo wa mfumu, wosunga akazi
ang'ono a mfumu; iyeyu sanakwanso kwa mfumu, koma
akakondwera naye mfumu, ndi kumuitana kumchula dzina lace,

ndiko. 15Pofika tsono kulowa kwace kwa Estere mwana wa Abihaili,
atate wamng'ono wa Moredekai, amene adadzitengera akhale
mwana wace, kuti alowe kwa mfumu, sanafuna kanthu koma
zonena Hege mdindo wa mfumu wosunga akazi ndizo. Ndipo
Estere anayamikizidwa pamaso pa onse ompenya. 16Momwemo
anatengedwa Estere kumka kwa mfumu Ahaswero, ku nyumba
yace yacifumu, mwezi wakhumi, ndiwo mwezi wa Tebete, caka
cacisanu ndi ciwiri ca ufumu wace. 17Ndipo mfumu inakonda Estere
koposa akazi onse, nalandira iye kuyanja ndi cifundo pamaso pace,
koposa anamwali onse; motero anaika korona wacifumu pamutu
pace, namuyesa mkazi wamkuru m'malo mwa Vasiti. 18Pamenepo
mfumu inawakonzera madyerero akuru ace onse, ndi omtumikira,
ndiwo madyerero a Estere; napumulitsa maiko, naninkha zaufulu
monga mwa ufulu wa mfumu. 19Ndipo posonkhanidwa anamwali
nthawi yaciwiri Moredekai anali wa m'bwalo la mfumu. 20Estere
sadaulula cibale cace kapena mtundu wace, monga Moredekai
adamuuza; popeza Estere anacita mau a Moredekai monga
m'mene analeredwa naye.

Moredekai aulula ciwembu cofuna kupha mfumu

21Masiku awa pokhala Moredekai wa m'bwalo la mfumu, Bigitana
ndi Teresi, adindo awiri a mfumu osunga pakhomo, anapsa mtima,
nayesa kumthira manja mfumu Ahaswero. 22Koma cidadziwika ici
kwa Moredekai, ndiye anafotokozera Estere mkazi wamkuru; ndi
Estere anamuuza mfumu, kumnenera Moredekai. 23Ndipo
atafunsira mlanduwo, anaupeza momwemo, napacikidwa onse
awiri pamtengo; ndipo anacilemba m'buku la mbiri pamaso pa
mfumu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Moredekai akana kugwadira Hamani

1Zitatha izi, mfumu Ahaswero anamkuza Hamani mwana wa
Hamedata, wa ku Agagi, namkweza, naika mpando wace upose
akalonga onse okhala naye. 2Ndipo anyamata onse a mfumu
okhala m'cipata ca mfumu anamweramira, namgwadira Hamani;
pakuti mfumu idalamulira cotero za iye. Koma Moredekai
sanamweramira kapena kumgwadira. 3Ndipo anyamata a mfumu
okhala m'cipata ca mfumu anati kwa Moredekai, Ulakwiranji pa
lamulo la mfumu? 4Kunali tsono, pomalankhula naye tsiku ndi
tsiku, osawamvera iye, anauza Hamani, kuona ngati mlandu wa
Moredekai udzakoma; popeza iye adawauza kuti ali Myuda. 5Ndipo
Hamani, pakuona kuti Moredekai sanamweramira kapena
kumgwadira, mtima wace unadzala mkwiyo. 6Koma anaciyesa
copepuka kumthira manja Moredekai yekha; pakuti
adamfotokozera mtundu wace wa Moredekai; potero Hamani
anafuna kuononga Ayuda lonse okhala m'ufumu wonse wa
Ahaswero, ndiwo a mtundu wa Moredekai.

Hamani apangira mfumu kuti uphedwe mtundu wonse wa Ayuda

7Mwezi woyamba ndiwo mwezi wa Nisani, caka cakhumi ndi ciwiri
ca mfumu Ahaswero, anaombeza Puri, ndiwo ula, pamaso pa
Hamani tsiku ndi tsiku, mwezi ndi mwezi, mpaka mwezi wakhumi
ndi ciwiri, ndiwo mwezi wa Adara. 8Ndipo Hamani anati kwa
mfumu Ahaswero, Pali mtundu wina wa anthu obalalika ndi
ogawanikana mwa mitundu ya anthu m'maiko onse a ufumu wanu,
ndi malamulo ao asiyana nao a anthu onse, ndipo sasunga
malamulo a mfumu; cifukwa cace mfumu siiyenera
kuwaleka. 9Cikakomera mfumu, cilembedwe kuti aononge iwo;
ndipo ndidzapereka matalente a siliva zikwi khumi m'manja a iwo
akusunga nchito ya mfumu, abwere nao kuwaika m'nyumba za
cuma ca mfumu. 10Ndipo mfumu inabvula mphete yace pa cala
cace, naipereka kwa Hamani mwana wa Hamedata wa ku Agagi,
mdani wa Ayuda. 11Ndipo mfumu idati kwa Hamani, Siliva akhale
wako, ndi anthu omwe; ucite nao monga momwe
cikukomera. 12Pamenepo anaitana alembi a mfumu mwezi
woyamba, tsiku lace lakhumi ndi citatu, nalembera monga mwa
zonse Hamani analamulira akazembe ndi ziwanga zoyang'anira
maiko ali onse, ndi akalonga a mitundu iri yonse ya anthu, maiko
ali onse monga mwa cilembedwe cao, ndi mitundu iri yonse ya
anthu monga mwa cinenedwe cao; anazilemba m'dzina la mfumu
Ahaswero, nazisindikiza ndi mphete ya mfumu. 13Ndipo anatumiza
akalata ndi amtokoma ku maiko onse a mfumu, kuti aononge,
aphe, napulule Ayuda onse, ndiwo ana, ndi okalamba, makanda,

ndi akazi, tsiku limodzi, ndilo tsiku lakhumi ndi citatu la mwezi wakhumi ndi ciwiri, ndiwo mwezi wa Adara; nalande zao mofunkha. 14Mau a colembedwaco, ndiwo kuti licitike lamulo m'maiko onse, analalikidwa kwa anthu onse, kuti akonzekeretu tsiku lomwelo. 15Amtokoma anaturuka ofulumizidwa ndi mau a mfumu, ndi lamulo linabukitsidwa m'cinyumba ca ku Susani; ndipo mfumu ndi Hamani anakhala pansi kumwa; koma mudzi wa Susani unadodoma.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Moredekai adandaulira Estere anenere Ayuda kwa mfumu

1Koma podziwa Moredekai zonse zidacitikazi, Moredekai
anang'amba zobvala zace, nabvala ciguduli ndi mapulusa,
naturuka pakati pa mudzi, napfuula, nalira kulira kwakukuru ndi
kowawa, 2nafika popenyana ndi cipata ca mfumu; popeza sanathe
munthu kulowa ku cipata ca mfumu wobvala ciguduli. 3Ndi
m'maiko monse, pali ponse anafikapo mau a mfumu ndi lamulo
lace, panali maliro akuru mwa Ayuda, ndi kusala, ndi kulira misozi,
ndi kubuma; nagona m'ciguduli ndi mapulusa ambiri. 4Ndipo
anamwali a Estere ndi adindo ace anadza, namuuza; ndi mkazi
wamkuru anawawidwa mtima kwambiri, natumiza cobvala abveke
Moredekai, ndi kumcotsera ciguduli cace; koma
sanacilandira. 5Pamenepo Estere anaitana Hataki mdindo wina wa
mfumu, amene idamuika amtumikire, namuuza amuke kwa
Moredekai, kuti adziwe ici nciani ndi cifukwa cace ninji. 6Naturuka
Hataki kumka kwa Moredekai ku khwalala la mudzi linali
popenyana ndi cipata ca mfumu. 7Ndipo Moredekai
anamfotokozera zonse zidamgwera, ndi mtengo wace wa ndarama
adati Hamani adzapereka m'nyumba ya cuma ca mfumu pa Ayuda,
kuwaononga. 8Anampatsanso citsanzo ca lamulo lolembedwa
adalibukitsa m'Susani, kuwaononga, acionetse kwa Estere, ndi
kumfotokozera, ndi kumlangiza alowe kwa mfumu, kumpembedza,
ndi kupempherera anthu ace kwa iye. 9Nadza Hataki, namuuza
Estere mau a Moredekai. 10Pamenepo Estere ananena ndi Hataki,
namtuma akauze Moredekai, ndi kuti, 11Akapolo onse a mfumu ndi
anthu a m'maiko a mfumu adziwa kuti ali yense, ngakhale
wamwamuna kapena wamkazi, akalowa kwa mfumu ku bwalo la
m'katimo wosaitanidwa, lamulo la pa iye ndi limodzi, ndilo kuti
amuphe, akapanda mfumu kumloza ndi ndodo yacifumu yagolidi
kuti akhale ndi moyo; koma ine sanaodiitana ndilowe kwa mfumu
masiku awa makumi atatu. 12Ndipo anamuuza Moredekai mau a
Estere. 13Koma Moredekai anawauza ambwezere mau Estere, kuti,
Usamayesa m'mtima mwako kuti udzapulumuka m'nyumba ya
mfumu koposa Ayuda onse ena. 14Pakuti ukakhala cete konse
tsopano lino, cithandizo ndi cipulumutso zidzafuma kwina; koma
iwe ndi nyumba ya atate wako mudzaonongeka; ndipo kaya,
kapena walowera ufumu cifukwa ca nyengo yonga iyi. 15Pamenepo
Estere anati ambwezere mau Moredekai, 16Muka, sonkhanitsa
Ayuda onse opezeka m'Susani, nimundisalire, osadya osamwa
masiku atatu, usiku ndi usana, ine ndemwe ndi anamwali anga
tidzasala momwemo, ndipo motero ndidzalowa kwa mfumu, ndiko
kosalingana ndi lamulo; ndikaonongeka tsono

ndionongeke, 17Napita Moredekai, nacita monga mwa zonse adamlamulira Estere.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Estere alowa kwa mfumu nampempha iye ndi Hamani azidya naye

1Ndipo kunali tsiku lacitatu, Estere anabvala zobvala zace
zacifumu, nakaimirira m'bwalo la m'kati la nyumba ya mfumu,
popenyana pa nyumba ya mfumu; ndi mfumu inakhala pa mpando
wace wacifumu m'nyumba yacifumu, pandunji polowera
m'nyumba. 2Ndipo kunali, pamene mfumu inaona Estere mkazi
wamkuruyo alikuima m'bwalo, inamkomera mtima; ndi mfumu
inamloza Estere ndi ndodo yacifumu yagolidi inali m'dzanja lace.
Nayandikira Estere, nakhudza nsonga ya ndodoyo. 3Ninena naye
mfumu, Mufunanji, Estere mkazi wamkuru? pempho lanu nciani?
lidzaperekedwa kwa inu, kufikira limodzi la magawo awiri a
ufumuwo. 4Ndipo Estere anati, Cikakomera mfumu, adze mfumu
ndi Hamani lero ku madyerero ndinawakonzera. 5Niti mfumu,
Mumfulumize Hamani, acitike mau a Estere. Nidza mfumu ndi
Hamani ku madyerero adawakonzera Estere. 6Ndipo mfumu inati
kwa Estere pa madyerero a vinyo, Pempho lanu nciani?
lidzaperekedwa kwa inu; mufunanji? cidzacitika, kufikira limodzi la
magawo awiri a ufumuwo. 7Nayankha Estere, nati, Pempho langa
ndi kufuna kwanga ndiko, 8ngati mfumu indikomera mtima,
ngatinso cakomera mfumu kupereka pempho langa ndi kucita
cofuna ine, adze mfumu ndi Hamani ku madyerero
ndidzawakonzera; ndipo mawa ndidzacita monga yanena mfumu.

Hamani amangitsa popacika Moredekai

9Ndipo Hamani anaturuka tsiku lomwelo wosekerera ndi
wokondwera mtima; koma pamene Hamani anapenya Moredekai
ku cipata ca mfumu, osamnyamukira kapena kumfumukira,
Hamani anadzazidwa ndi mkwiyo pa Moredekai. 10Koma Hamani
anadziletsa, namuka kwao, natumiza munthu kukatenga mabwenzi
ace, ndi Zeresi mkazi wace. 11Nawawerengera Hamani kulemera
kwace kwakukuru, ndi ana ace ocuruka, ndi zonse mfumu
idamkuza nazo, ndi umo adamkweza koposa akalonga ndi
anyamata a mfumu. 12Hamani anatinso, Ndiponso Estere mkazi
wamkuru sanalola mmodzi yense alowe pamodzi ndi mfumu ku
madyerero adakonzawo, koma ine ndekha; nandiitana mawanso
pamodzi ndi mfumu. 13Koma zonsezi sindipindula nazo kanthu
konse, pokhala ndirikuona Moredekai Myudayo alikukhala ku cipata
ca mfumu. 14Pamenepo Zeresi mkazi wace, ndi mabwenzi ace
onse ananena naye, Apange mtengo, msinkhu wace mikono
makumi asanu, ndi mawa mukanene nayo mfumu kuti ampacike
Moredekai pamenepo; nimulowe pamodzi ndi mfumu kumadyerero
wokondwera. Ndipo ici cidakomera Hamani, napangitsa anthu
mtengowo.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Ahaswero aona cifukwa ca kucitira Moredekai ulemu

1Usiku uja tulo tidamwazikira mfumu, niti abwere nalo buku la
mbiri, naliwerenga pamaso pa mfumu. 2Napeza mudalembedwa
kuti Moredekai adaulula za Bigitana ndi Teresi, awiri a adindo a
mfumu osunga pakhomo, amene adayesa kumthira manja mfumu
Ahaswero. 3Niti mfumu, Anamcitira Moredekai ulemu ndi ukulu
wotani cifukwa ca ici? Ndipo anyamata a mfumu akuitumikira
ananena nayo, Sanamcitira kanthu. 4Niti mfumu, Ali kubwalo
ndani? Koma Hamani adalowa m'bwalo lakunja la nyumba ya
mfumu kulankhula ndi mfumu za kupacika Moredekai pamtengo
adaukonzeratu. 5Ndipo anyamata a mfumu ananena nayo,
Taonani, Hamani alikuima pabwalo. Niti mfumu, Alowe. 6Nalowa
Hamani. Ndipo mfumu inati kwa iye, Kodi amcitire ciani munthu
amene mfumu ikondwera kumcitira ulemu? Ndipo Hamani anati
mumtima mwace, Ndaniyo mfumu ikondwera kumcitira ulemu
koposa ine? 7Nati Hamani kwa mfumu, Munthu amene mfumu
ikondwera kumcitira ulemu, 8amtengere cobvala cacifumu
amacibvala mfumu, ndi kavalo amakwerapo mfumu, naike korona
wacifumu pamutu pace, 9napereke cobvala ndi kavalo m'dzanja la
wina womveketsa wa akalonga a mfumu, nabveke naco munthu
amene mfumu ikondwera kumcitira ulemu, namuyendetse pa
kavaloyo m'khwalala la m'mudzi, napfuule pamaso pace, Azitero
naye munthu amene mfumu ikondwera kumcitira
ulemu. 10Pamenepo mfumu inati kwa Hamani, Fulumira, tenga
cobvala ndi kavalo monga umo wanenera, nucitire cotero
Moredakai Myudayo, wokhala pa cipata ca mfumu; kasasowepo
kanthu ka zonse wazinena. 11Ndipo Hamani anatenga cobvala ndi
kavalo, nabveka Moredekai, namuyendetsa pa kavalo m'khwalala
la m'mudzi, napfuula pamaso pace, Azitero naye munthu amene
mfumu ikondwera kumcitira ulemu. 12Ndipo Moredekai
anabweranso ku cipata ca mfumu. Koma Hamani anafulumira
kumka kwao, wacisoni ndi wopfunda mutu wace. 13Ndipo Hamani
anafotokozera Zeresi mkazi wace, ndi mabwenzi ace onse, zonse
zidamgwera, Nanena naye anzeru ace, ndi Zeresi mkazi wace,
Moredekai amene wayamba kutsika pamaso pace, akakhala wa
mbumba ya Ayuda, sudzamlaka; koma udzagwada pamaso
pace. 14Akali cilankhulire naye, anafika adindo a mfumu,
nafulumira kumtenga Hamani kumka naye kumadyerero
adawakonzera Estere.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Hamani aululidwa napacikidwa

1Motero inadza mfumu ndi Hamani kumwa naye mkazi wamkuru
Estere. 2Nitinso mfumu kwa Estere tsiku laciwirili pa madyerero a
vinyo, Pempho lanu nciani, mkazi wamkuru Estere? lidzapatsidwa
kwa inu; mufunanji? cidzacitika, kufikira limodzi la magawo awiri a
ufumu wanga. 3Nayankha mkazi wamkuru Estere, nati, Ngati
mwandikomera mtima, mfumu, ndipo cikakomera mfumu,
andilekere moyo wanga pa kupempha kwanga, ndi wa anthu a
mtundu wanga pa pempho langa; 4pakuti tagulitsidwa; ine ndi
anthu amtundu wanga, kuti ationonge, atiphe, natipulule, Koma
tikadagulitsidwa tikhale akapolo ndi adzakazi, ndikadakhala cete;
cinkana wosautsa sakadakhoza kubwezera kusowa kwa
mfumu. 5Pamenepo mfumu Ahaswero inalankhula, niti kwa mkazi
wamkuru Estere, Ndani uyu, ali kuti iyeyu wadzazidwa mtima wace
kuti azitero? 6Nati Estere, Munthu wosautsa ndi mdani ndiye
Hamani woipa uyu. Pamenepo Hamani anagwidwa mantha pamaso
pa mfumu ndi mkazi wamkuru. 7Ninyamuka mfumu mu mkwiyo
wace ku madyerero a vinyo, nimka ku munda wa maluwa wa
kucinyumba; koma Hamani anatsalira kudzipempherera moyo kwa
mkazi wamkuru Estere; popeza anapenya kuti mfumu inatsimikiza
mtima kumcitira coipa. 8Nibwera mfumu ku munda wa maluwa wa
kucinyumba kulowanso m'nyumba munali madyerero a vinyo,
napeza Hamani atagwa pa kama wokhalapo Estere. Niti mfumu,
Kodi aumiriza mkazi wamkuru pamaso panga m'nyumba? Poturuka
mau pakamwa pa mfumu anamphimba Hamani nkhope. 9Nati
Haribona wina wa adindo okhala pamaso pa mfumu, Taonaninso,
mtengowo msinkhu wace mikono makumi asanu, umene Hamani
anaupangira Moredekai wonenera mfumu zokoma, uimiritsidwa
m'nyumba ya Hamani. Niti mfumu, Mpacike
pomwepo. 10Nampacika Hamani pa mtengo adaukonzera
Moredekai. Pamenepo mkwiyo wa mfumu unatsika.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Ahaswero abvomereza pempho la Estere, Ayuda napulumuka

1Tsiku lomwelo mfumu Ahaswero anampatsa mkazi wamkuru
Estere nyumba ya Hamani mdani wa Ayuda, Nafika Moredekai
pamaso pa mfumu; pakuti Estere adamuuza za cibale cace. 2Ndipo
mfumu inabvula mphete yace adailanda kwa Hamani, naipereka
kwa Moredekai. Ndi Estere anaika Moredekai akhale woyang'anira
nyumba ya Hamani. 3Nanenanso Estere pamaso pa mfumu, nagwa
ku mapazi ace, nalira misozi, nampembedza kuti acotse coipaco ca
Hamani wa ku Agagi, ndi ciwembu adacipangira Ayuda, 4Ndipo
mfumu inaloza Estere ndi ndodo yacifumu yagolidi. Nanyamuka
Estere, naima pamaso pa mfumu. 5Nati, Cikakomera mfumu, ndipo
ngati yandikomera mtima, niciyenera kwa mfumu, ngatinso
ndimcititsa kaso, alembere cosintha mau a akalata a ciwembu ca
Hamani mwana wa Hamedata wa ku Agagi, amene adawalembera
kuononga Ayuda okhala m'maiko onse a mfumu; 6pakuti
ndidzapirira bwanji pakuciona coipa cirikudzera amtundu wanga,
kapena ndidzapirira bwanji pakuciona cionongeko ca pfuko
langa? 7Pamenepo mfumu Ahaswero anati kwa mkazi wamkuru
Estere, ndi kwa Moredekai Myuda, Taonani, ndampatsa Estere
nyumba ya Hamani, ndi iyeyu anampacika pamtanda, cifukwa
anaturutsa dzanja lace pa Avuda, 8Mulembere inunso kwa Ayuda
monga mufuna, m'dzina la mfumu, nimusindikize ndi mphete ya
mfumu; pakuti kalata wolembedwa m'dzina la mfumu, ndi
kusindikizika ndi mphete ya mfumu, palibe munthu akhoza
kumsintha. 9Pamenepo anaitana alembi a mfumu nthawi
yomweyo, mwezi wacitatu, ndiwo mwezi wa Sivani, tsiku lace la
makumi awiri ndi citatu, monga mwa zonse Moredekai
analamulira; nalembera kwa Ayuda ndi kwa akazembe, ndi
ziwanga, ndi akalonga a kumaiko, oyambira ku Indiya, ofikira ku
Kusi, maiko zana limodzi mphambu makumi awiri kudza asanu ndi
awiri, ku dziko liri lonse monga mwa cilembedwe cao, ndi mtundu
uli wonse monga mwa cinenedwe cao, ndi kwa Ayuda monga mwa
cilembedwe cao, ndi monga mwa cinenedwe cao. 10Ndipo
analembera m'dzina la mfumu Ahaswero, nasindikiza ndi mphete
ya mfumu, natumiza akalata ndi amtokoma pa akavalo, okwera pa
akavalo aliwiro acifumu, obadwa mosankhika; 11m'menemo
mfumu inalola Ayuda okhala m'midzi iri yonse asonkhane, ndi
kulimbikira moyo wao, kuononga, kupha, ndi kupulula mphamvu
yonse ya anthu ndi ya dziko yofuna kuwathira nkhondo, iwo, ana
ang'ono ao, ndi akazi ao, ndi kulanda zofunkha zao, 12tsiku
lomwelo, m'maiko onse a mfumu Ahaswero, tsiku lakhumi ndi
citatu la mwezi wakhumi ndi ciwiri, ndiwo mwezi wa

Adara. 13Citsanzo cace, ca lemboli, cakuti abukitse lamulo m'maiko
onse, cinalalikidwa kwa mitundu yonse ya anthu, kuti, Ayuda
akonzekeretu tsiku lijalo, kubwezera cilango adani ao. 14Naturuka
amtokoma okwera pa akavalo aliwiro acifumu; pakuti mau a
mfumu anawafulumiza ndi kuwaumiriza; ndipo lamulolo
linabukitsidwa m'cinyumba ca ku Susani. 15Ndipo Moredekai
anaturuka pamaso pa mfumu wobvala cobvala cacifumu camadzi
ndi coyera, ndi korona wamkuru wagolidi, ndi maraya abafuta ndi
ofiirira; ndi mudzi wa Susani unapfuula ndi kukondwera. 16Ayuda
anali nako kuunika, ndi kukondwera, ndi cimwemwe, ndi
ulemu. 17Ndi m'maiko monse, ndi m'midzi yonse, mudafika mau a
mfumu ndi lamulo lace, Ayuda anali nako kukondwera ndi
cimwemwe, madyerero ndi tsiku lokoma. Ndipo ambiri a mitundu
ya anthu a m'dziko anasanduka Ayuda; pakuti kuopsa kwa Ayuda
kudawagwera.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Ayuda awapha adani ao

1Mwezi wakhumi ndi ciwiri tsono, ndiwo mwezi wa Adara, tsiku lace
lakhumi ndi citatu, mau a mfumu ndi lamulo lace ali pafupi
kucitika, tsikuli adani a Ayuda anayesa kuwacitira ufumu, koma
cinasinthika; popeza Ayuda anacitira ufumu iwo odana nao; 2pakuti
Ayuda anasonkhana pamodzi m'midzi mwao, m'maiko onse a
mfumu Ahaswero, kuwathira manja ofuna kuwacitira coipa, ndipo
palibe munthu analimbika pamaso pao; popeza kuopsa kwao
kudawagwera mitundu yonse ya anthu. 3Ndipo akalonga onse a
maikowo, ndi akazembe, ndi ziwanga, ndi iwo ocita nchito ya
mfumu, anathandiza Ayuda; popeza kuopsa kwa Moredekai
kudawagwera. 4Pakuti Moredekai anali wamkuru m'nyumba ya
mfumu, ndi mbiri yace idabuka m'maiko onse; pa kuti munthuyu
Moredekai anakula-kulabe. 5Ndipo Ayuda anakantha adani ao onse,
kuwakantha ndi lupanga, ndi kuwapulula, nacitira odana nao
monga anafuna. 6Ndipo m'cinyumba ca ku Susani Ayuda
anakantha, naononga amuna mazana asanu. 7Napha Parisandata,
ndi Dalifoni, ndi Asipata, 8ndi Porata, ndi Adaliya, ndi Aridata, 9ndi
Parimasta, ndi Arisai, ndi Aridai, ndi Vaisata, 10ana amuna khumi a
Hamani mwana wa Hamedata, mdani wa Ayuda. Koma sanalanda
zofunkha. 11Tsiku lomwelo anabwera naco kwa mfumu ciwerengo
ca iwo ophedwa m'cinyumba ca ku Susani. 12Ndipo mfumu inati
kwa mkazi wamkuru Estere, Ayuda adapha, naononga amuna
mazana asanu m'cinyumba ca ku Susani, ndi ana amuna khumi a
Hamani; nanga m'maiko ena a mfumu munacitikanji? pempho lanu
ndi ciani tsono? lidzacitikira inu; kapena mufunanjinso?
kudzacitika. 13Nati Estere, Cikakomera mfumu, alole Ayuda okhala
m'Susani acite ndi mawa lomwe monga mwa lamulo la lero; ndi
ana amuna khumi a Hamani apacikidwe pamtengo. 14Ndipo
mfumu inati azicita motero, nalamulira m'Susani, napacikidwa ana
amuna khumi a Hamani. 15Ndipo Ayuda okhala m'Susani
anasonkhana pamodzi, tsiku lakhumi ndi cinai la mwezi wa Adara,
napha amuna mazana atatu m'Susani; koma sanalanda
zofunkha. 16Nasonkhana pamodzi Ayuda ena okhala m'maiko a
mfumu, nalimbikira moyo wao, napumula pa adani ao, nawapha a
iwo odana nao zikwi makumi asanu ndi awiri mphambu zisanu;
koma sanalanda zofunkha. 17Cinacitika ici tsiku lakhumi ndi citatu
la mwezi wa Adara, ndi tsiku lace lakhumi ndi cinai anapumula,
naliyesa tsiku lamadyerero ndi lakukondwesa. 18Koma Ayuda
okhala m'Susani anasonkhana tsiku lace lakhumi ndi citatu ndi
lakhumi ndi cinai, ndi pa tsiku lakhumi ndi cisanu anapumula,
naliyesa tsiku lamadyerero ndi lakukondwera. 19Cifukwa cace
Ayuda a kumiraga, okhala m'midzi yopanda malinga, amaliyesa

tsiku lakhumi ndi cinai la mwezi wa Adara tsiku la kukondwera ndi madyerero, ndi tsiku lokoma, ndi lakutumizirana magawo.

Masungidwe a tsiku la Purimu

20Ndipo Moredekai analembera izi, natumiza akalata kwa Ayuda onse okhala m'maiko onse a mfumu Ahaswero, a kufupi ndi a kutali, 21kuwalimbikitsira, asunge tsiku lakhumi ndi cinai, mwezi wa Adara, ndi tsiku lace lakhumi ndi cisanu lomwe, caka ndi caka, 22ndiwo masiku amene Ayuda anapumula pa adani ao; ndi mwezi wacisoni unawasandulikira wakukondwera, ndi wamaliro ukhale tsiku lokoma, awayese masiku amadyerero ndi akukondwera, akutumizirana magawo, ndi akupatsa zaufulu kwa osauka. 23Ndipo Ayuda anabvomereza kucita monga umo adayambira, ndi umo Moredekai adawalembera; 24popeza Hamani mwana wa Hamedata wa ku Agagi, mdani wa Ayuda onse, adapangira Ayuda ciwembu kuwaononga, naombeza Puri, ndiwo ula, kuwatha ndi kuwaononga; 25koma pofika mlanduwo kwa mfumu, anati mwa akalata kuti ciwembu cace coipa adacipangira Ayuda, cimbwerere mwini; ndi kuti Iye ndi ana amuna ace apacikidwe pamtengo, 26Cifukwa cace anacha masikuwa Purimu, ndilo dzina la ulawo. Momwemo, cifukwa ca mau onse a kalatayo, ndi izi adaziona za mlanduwo, ndi ici cidawadzera, 27Ayuda anakhazikitsa ici, nadzilonjezetsa okha, ndi mbeu yao, ndi onse akuphatikana nao, cingalekeke, kuti adzasunga masiku awa awiri monga mwalembedwa, ndi monga mwa nyengo yao yoikika, caka ndi caka; 28ndi kuti masikuwa adzakumbukika ndi kusungika mwa mibadwo yonse, banja liri lonse, dziko liri lonse, ndi mudzi uli wonse; ndi kuti masiku awa sadzalekeka mwa Ayuda, kapena kusiyidwa cikumbukilo cao mwa mbeu yao. 29Pamenepo Estere mkazi wamkuru mwana wa Abihaili, ndi Moredekai Myuda, analembera molamulira, kukhazikitsa kalata uyu waciwiri wa Purimu. 30Natumiza iye akalata kwa Ayuda onse, ku maiko zana limodzi mphambu makumi awiri kudza asanu ndi awiri a ufumu wa Ahaswero, ndiwo mau a mtendere ndi coonadi; 31kukhazikitsa masiku awa a Purimu m'nyengo zao, m'mene Moredekai Myuda ndi mkazi wamkuru Estere adawakhazikitsira; ndi umo anadzikhazikitsira okha, ndi mbeu yao, kunena za kusala kwao, ndi kupfuula kwao. 32Ndipo kunena kwace kwa Estere kunakhazikitsa mau awa a Purimu; ndipo kunalembedwa m'buku.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Ukuru wa Moredekai

1Ndipo mfumu Ahaswero inasonkhetsa dziko, ndi zisumbu za ku nyanja
yamcere. 2Ndi zocita zonse za mphamvu yace, ndi nyonga zace, ndi
mafotokozedwe a ukulu wa Moredekai, umene mfumu inamkulitsa nao,
sizilembedwa kodi m'buku la mbiri ya mafumu a Mediya ndi Perisiya? 3Pakuti
Moredekai Myuda anatsatana naye mfumu Ahaswero, nakhala wamkuru mwa
Ayuda, nabvomerezeka mwa unyinji wa abale ace wakufunira a mtundu wace
zokoma, ndi wakunena za mtendere kwa mbeu yace yonse.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Job

Yobu 1

Yobu wosautsidwabe alimbika kutama Mulungu

1PANALI munthu m'dziko la Uzi, dzina lace ndiye Yobu; ndipo munthuyu anali
wangwiro ndi woongoka, wakuopa Mulungu ndi kupewa zoipa. 2Ndipo anabala
ana amuna asanu ndi awiri, ndi ana akazi atatu. 3Zoweta zacenso zinali
nkhosa zikwi zisanu ndi ziwiri, ndi ngamila zikwi zitatu, ndi ng'ombe zamagoli
mazana asanu, ndi aburu akazi mazana asanu, anchito ace omwe ndi ambiri;
cotero munthuyu anaposa anthu onse'a kum'mawa. 4Ndipo ana ace amuna
anamuka kukacita madyerero m'nyumba ya yense pa tsiku lace; natumiza
mthenga kuitana alongo ao atatu adzadye nadzamwe nao. 5Ndipo kunatero,
atatha masiku a madyererowa Yobu anatumiza mau, nawapatula, nauka
mamawa, nafukiza nsembe zopsereza, monga mwa kuwerenga kwa iwo onse;
pakuti Yobu anati, Kapena anacimwa ana anga, nacitira Mulungu mwano
m'mtima mwao. Anatero Yobu masiku onse.
6Ndipo panali tsiku lakuti ana a Mulungu anadza kudzionetsa kwa Yehova,
nadzanso Satana pakati pao. 7Nati Yehova kwa Satana, Ufuma kuti? Nayankha
Satana kwa Yehova, nati, Kupitapita m'dziko ndi kuyendayenda
m'mwemo. 8Ndipo Yehova anati kwa Satana, Kodi waonerera mtumiki wanga
Yobu? pakuti palibe wina wonga iye m'dzikomo, munthu wangwiro ndi
woongoka, wakuopa Mulungu ndi kupewa zoipa. 9Nayankha Satana, nati kwa
Yehova, Kodi Yobu aopa Mulungu pacabe? 10Kodi simunamcinga iye ndi
nyumba yace, ndi zace zonse, pomzinga ponse? nchito ya manja ace
mwaidalitsa, ndi zoweta zace zacuruka m'dziko. 11Koma mutambasule dzanja
lanu ndi kumkhudzira zace zonse, ndipo adzakucitirani mwano pankhope
panu. 12Nati Yehova kwa Satana, Taona, zonse ali nazo zikhale m'dzanja
mwako; pa iye pokha usatambasula dzanja lako. Naturuka Satana pamaso pa
Yehova.
13Tsono panali tsiku loti ana ace amuna ndi akazi analinkudya ndi kumwa
vinyo m'nyumba ya mkuru wao; 14nafika mthenga kwa Yobu, nati, Ng'ombe
zinalikulima, ndi aburu akazi analikudya pambali pao; 15koma anazigwera
Aseba, nazitenga, nawapha anyamata ndi lupanga lakuthwa, ndipo
ndapulumuka ine ndekha kudzakuuzani. 16Akali cilankhulire uyu, anadza
winanso, nati, Wagwa moto wa Mulungu wocokera kumwamba, wapsereza
nkhosa ndi anyamata, nuzinyeketsa; ndipo ndapulumuka ine ndekha
kudzakuuzani. 17Akali cilankhulire uyu, anadza winanso, nati, Akasidi
anadzigawa magulu atatu, nazigwera ngamila, nazitenga, nawapha anyamata
ndi lupanga lakuthwa, ndipo ndapulumuka ine ndekha kudzakuuzani. 18Akali
cilankhulire, anadza winanso, nati, Ana anu amuna ndi akazi analinkudya ndi
kumwa vinyo m'nyumba ya mkuru wao; 19ndipo taonani, inadza mphepo
yaikuru yocokera kucipululu, niomba pa ngondya zonse zinai za nyumbayo,
nigwa pa anyamatawo, nafa; ndipo ndapulumuka ine ndekha
kudzakuuzani. 20Pamenepo Yobu ananyamuka, nang'amba maraya ace,
nameta mutu wace, nagwa pansi, nalambira, 21nati, Ndinaturuka m'mimba ya
mai wanga wamarisece, wamarisece ndidzanrukanso; Yehova anapatsa,
Yehova watenga, lidalitsike dzina la Yehova. 22Mwa ici conse Yobu sanacimwa,
kapena kunenera Mulungu colakwa.

©The Bible Society of Malawi, 1992

1Panalinso tsiku lakuti anadza ana a Mulungu kudzionetsa kwa
Yehova, nadza Satana yemwe pakati pao kudzionetsa kwa
Yehova. 2Ndipo Yehova anati kwa Satana, Ufuma kuti? Nayankha
Satana, nati kwa Yehova, Kupitapita m'dziko, ndi kuyendayenda
m'mwemo. 3Ndipo Yehova anati kwa Satana, Kodi waonerera
mtumiki wanga Yobu? pakuti palibe wina wonga iye m'dzikomo,
munthu wangwiro ndi woongoka, wakuopa Mulungu, ndi kupewa
zoipa; naumirirabe kukhala wangwiro, cinkana undisonkhezera
ndimuononge kopanda cifukwa. 4Nayankha Satana, nati kwa
Yehoya, Khungu kulipa khungu, inde munthu adzapereka zonse ali
nazo kuombola moyo wace. 5Koma tambasulani dzanja lanu, ndi
kukhudza pfupa lace ndi mnofu wace, ndipo adzakucitirani mwano
pamaso panu. 6Ndipo Yehova anati kwa Satana. Taona, akhale
m'dzanja lako; moyo wace wokha uuleke. 7Naturuka Satana pamaso
pa Yehova, nazunza Yobu ndi zironda zowawa, kuyambira ku phazi
lace kufikira pakati pamutu pace. 8Ndipo anadzitengera phale,
kudzikanda nalo; nakhala pansi m'mapulusa. 9Pamenepo mkazi
wace ananena naye, Kodi uumiriranso kukhala wangwiro? citira
Mulungu mwano, ufe. 10Koma ananena naye, Ulankhula monga
amalankhula akazi opusa. Ha! tidzalandira zokoma kwa Mulungu
kodi, osalandiranso zoipa? pa ici conse Yobu sanacimwa ndi milomo
yace.

Mabwenzi ace atatu adzaceza naye

11Atamva tsono mabwenzi atatu a Yobu za coipa ici conse
cidamgwera, anadza, yense kucokera kwao, Elifazi wa ku Temani,
ndi Bilidadi Msuki, ndi Zofari wa ku Naama, napangana kudzafika
kumlirira ndi kumsangalatsa. 12Ndipo pokweza maso ao ali kutali,
sanamdziwa, nakweza mau ao, nalira; nang'amba yense maraya
ace, nawaza pfumbi kumwamba ligwe pamitu pao. 13Nakhala pansi
pamodzi naye panthaka masiku asanu ndi awiri usana ndi usiku,
palibe mmodzi ananena naye kanthu, popeza anaona kuti
kuwawaku nkwakukuru ndithu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Madandaulo a Yobu

1Atatero, Yobu anatsegula pakamwa pace, natemberera tsiku lace.
2Nalankhula Yobu nati,
3Litayike tsiku lobadwa ine,
Ndi usikuwo udati, Waima naye mwana wamwamuna.
4Tsiku lija likhale mdima;
Mulungu asalifunse kumwamba,
Ndi kuunika kusaliwalire.
5Mdima ndi mthunzi wa imfa ziliyese lao lao;
Mtambo ulikhalire;
Zonse zodetsa usana bi ziliopse.
6Usiku uja, mdima weni weni uugwere;
Usakondwerere mwa masiku a m'caka;
Usalowe m'ciwerengedwe ca miyezi.
7Ha! usiku uja ukhale cumba;
Kuyimbira kokondwera kusalowem'mwemo.
8Autemberere iwo akutemberera usana,
Odziwa kuutsa cinjokaco.
9Nyenyezi za cizirezire zide;
Uyembekezere kuunika, koma kuusowe;
Usaone kuphenyuka kwa mbanda kuca;
10Popeza sunatseka pa makomo ace mimba ya mai wanga.
Kapena kundibisira mabvuto pamaso panga.
11Ndinalekeranji kufera m'mimba?
Ndi kupereka mzimu wanga pobadwa ine?
12Anandilandiriranji maondo?
Kapena mabere kuti ndiyamwe?
13Pakuti ndikadagona pansi pomwepo ndi kukhala cete;
Ndikanagona tulo; pamenepo ndikadaona popumula;
14Pamodzi ndi mafumu ndi maphungu a padziko,
Akudzimangira m'mabwinja;
15Kapena pamodzi ndi akalonga eni ace a golidi,
Odzaza nyumba zao ndi siliva;
16Kapena ngati nsenye yobisika ndikadakhala kuli zi;
Ngati makanda osaona kuunika.
17Apo oipa aleka kumabvuta;
Ndi apo ofoka mphamvu akhala m'kupumula.
18Apo a m'kaidi apumula pamodzi,
Osamva mau a wofulumiza wao.
19Ang'ono ndi akulu ali komwe;
Ndi kapolo amasuka kwa mbuyace.
20Amninkhiranji kuunika wobvutika,
Ndi moyo kwa iye wakuwawa mtima,

21Wakuyembekezera imfa, koma kuli zi,
Ndi kuikumba koposa cuma cobisika,
22Wakusekerera ndi cimwemwe
Ndi kukondwera pakupeza manda?
23Amuonetseranji kuunika munthu wa njira yobisika,
Amene wamtsekera Mulungu?
24Pakuti ndikati ndidye, kumadza kuusa moyo kwanga;
Ndi kudzuma kwanga kumathiridwa ngati madzi.
25Pakuti cimene ndinaciopa candigwera,
Ndi cimene ndacita naco mantha candidzera.
26Wosakhazikika, ndi wosakhala cete, ndi wosapumula ine,
Koma mabvuto anandidzera.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Elifazi adzudzula Yobu; tsoka la munthu licokera ku zoipa zace; Yobu alape

1 Pamenepo Elifazi wa ku Temani anayankha, nati,
2 Munthu akayesa kunena nawe mau, kodi udzamva nao cisoni?
Koma akhoza ndani kudziletsa kunena?
3 Taona iwe walangiza aunyinji,
Walimbitsa manja a ofoka.
4 Mau ako anacirikiza iye amene akadagwa,
Walimbitsanso maondo otewa.
5 Koma tsopano cakufikira iwe, ndipo ukomoka;
Cikukhudza, ndipo ubvutika.
6 Kodi kulimbika mtima kwako si ndiko kuti uopa Mulungu,
Ndi ciyembekezo cako si ndiwo ungwiro wa njira zako?
7 Takumbukila tsopano, watayika ndani wosaparamula konse?
Kapena oongoka mtima alikhidwa kuti?
8 Monga umo ndaonera, olimira mphulupulu,
Nabzala bvuto, akololapo zomwezo.
9 Atayika ndi mpweya wa Mulungu,
Nathedwa ndi mpumo wa mkwiyo wace.
10 Kubangula kwa mkango, ndi kulira kwa mkango waukali kwaletsedwa,
Ndi mano a misona ya mkango atyoledwa.
11 Mkango wokalamba udzifera posowa mkoka,
Ndi misona ya mkango waukazi imwazika.
12 Anditengera mau m'tseri,
M'khutu mwanga ndinalandira kunong'oneza kwace.
13 M'malingaliro a masomphenya a usiku,
Powagwira anthu tulo tatikuru,
14 Anandidzera mantha ndi kunjenjemera,
Nanthunthumira nako mafupa anga onse.
15 Pamenepo panapita mzimu pamaso panga;
Tsitsi la thupi langa lidati nyau nyau.
16 Unaima ciriri, koma sindinatha kuzindikira maonekedwe ace;
Panali mzukwa pamaso panga;
Kunali cete, ndipo ndidamva mau akuti,
17 Kodi munthu adzakhala wolungama ndi kuposa Mulungu?
Kodi munthu adzakhala woyera woposa Mlengi wace?
18 Taona, sakhulupirira atumiki ace;
Nawanenera amithenga ace zopusa;
19 Kopambana kotani nanga iwo akukhala m'nyumba zadothi,
Amene kuzika kwao kuti m'pfumbi,
Angothudzulidwa ngati gulugufe,
20 Kuyambira m'mawa kufikira madzulo athudzuka;

Aonongeka kosatha, osasamalirako munthu.
21Kukometsetsa kwao sikumacotsedwa nao?
Amafa koma opanda nzeru.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Yobu 5
1Itana tsono; pali wina wakukuyankha kodi?
Ndipo udzatembenukira kwa yani wa oyera mtimawo?
2Pakuti mkwiyo umapha wopusa,
Ndi nsanje imakantha wopanda pace.
3Ndinapenya wopusa woyala mizu;
Koma pomwepo ndinatemberera pokhala pace.
4Ana ace akhala otekeseka, Napsinjika kucipata,
Wopanda wina wakuwapulumutsa.
5Zokolola zao anjala azidya,
Azitenga ngakhale kuminga,
Ndi aludzu ameza cuma cao.
6Pakuti nsautso siituruka m'pfumbi,
Ndi mabvuto saphuka m'nthaka;
7Koma munthu abadwira mabvuto,
Monga mbaliwali zikwera ziuluzika.
8Koma ine ndikadafuna Mulungu,
Ndikadaikira mlandu wanga Mulungu;
9Amene acita zazikuru ndi zosalondoleka,
Zinthu zodabwiza zosawerengeka.
10Amene abvumbitsa mvula panthaka,
Natumiza madzi paminda;
11Kuika opeputsidwa pamalo ponyamuka,
Kuti iwo a maliro akwezedwe posatekeseka.
12Apititsa pacabe ziwembu za ocenjerera,
Kuti manja ao sakhoza kucita copangana cao.
13Akola eni nzeru m'kucenjerera kwao,
Ndi uphungu wa opotoka mtima usonthokera pacabe,
14Iwo akomana ndi mdima pali dzuwa,
Nayambasa dzuwa liri pakati pamtu monga usiku.
15Apulumutsa aumphawi ku lopanga
La kukamwa kwao, ndi ku dzanja la wamphamvu.
16Potero aumphawi ali naco ciyembekezo,
Ndi mphulupulu yatsekedwa pakamwa.
17Taona, wodala munthu amene Mulungu amdzudzula;
Cifukwa cace usapeputsa kulanga kwa Wamphamvuyonse.
18Pakuti apweteka, namanganso mabala;
Alasa, ndi manja ace omwe apoletsa.
19Adzakupulumutsa m'masautso asanu ndi limodzi;
Cinkana mwa asanu ndi awiri palibe coipa cidzakukhudza.
20Adzakuombola kuimfa m'njala,
Ndi ku mphamvu ya lupanga m'nkhondo.
21Udzabisikira mkwapulo wa lilime,
Sudzaciopanso cikadza cipasuko.

22Cipasuko ndi njala udzaziseka;
Ngakhale zirombo za padziko osaziopa.
23Pakuti udzakhala ndi pangano ndi miyala ya kuthengo;
Ndi nyama za kuthengo zidzakhala nawe mumtendere.
24Ndipo udzapeza kuti pahema pako mpa mtendere;
Nudzazonda za m'banja mwako osasowapo kanthu,
25Udzapezanso kuti mbeu zako zidzacuruka,
Ndi obala iwe ngati zitsamba za padziko.
26Udzafika kumanda utakalamba,
Monga abwera nao mtolo wa tirigu m'nyengo yace.
27Taona, ici tacifunafuna, ciri catero;
Ucimvere, nucidziwire wekha.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Yobu akuti ali ndi cifukwa ca kudandaula, alira kufa, adzuzula mabwenzi pa kuuma mtima kwao, apempha Mulungu amcitire cifundo

1Koma Yobu anayankha, nati,
2Mwenzi atayesa bwino cisoni canga,
Ndi kuika matsoka anga pamodzi pamuyeso!
3Pakuti zikadalemera tsopano koposa mcenga wa kunyanja;
Cifukwa cace mau anga ndasonthokera kunena.
4Pakuti mibvi ya Wamphamvuyonse yandilowa,
Mzimu wanga uumwa ulembe wace;
Zoopsa za Mulungu zindindandira nkhondo.
5Kodi mbidzi ilira pokhala nao msipu?
Ilira kodi ng'ombe pa cakudya cace?
6Kodi cinthu cosakolera cidyeka copanda mcere?
Coyera ca dzira cikolera kodi?
7Zimene moyo wanga ukana kuzikhudza
Zikunga cakudya cosakolera kwa ine.
8Ha! ndikadakhala naco cimene ndicipempha,
Mulungu akadandipatsa cimene ndicilira!
9Cimkomere Mulungu kundiphwanya,
Alole dzanja lace lindilikhel
10Pamenepo ndidzasangalala,
Ndidzakondwera naco cowawa cosandileka;
Pakuti sindinawabisa mau a Woyerayo.
11Mphamvu yanga njotani kuti ndiyembekeze?
Mathedwe anga ndi otani kuti ndipirire?
12Kodi mphamvu yanga ndiyo mphamvu ya miyala?
Mnofu wanga ndi mkuwa kodi?
13Mulibe thandizo mwa ine ndekha; cipulumutso candithawa.
14Iye amene akadakomoka, bwenzi lace ayenera kumcitira cifundo;
Angaleke kuopa Wamphamvuyonse.
15Abale anga anacita monyenga ngati kamtsinje,
Ngati madzi a timitsinje akupitirira.
16Amada cifukwa ca madzi oundana.
M'menemo cipale cofewa cibisika;
17Atafikira mafundi, mitsinje iuma;
Kukatentha, imwerera m'malo mwao.
18Aulendo akutsata njira yao apambukapo,
Akwerera poti se, natayika.
19Aulendo a ku Tema anapenyerera,
Makamu a ku Seba anaiyembekezera.
20Anazimidwa popeza adaikhulupirira;
Anafikako, nathedwa nzeru.

21Pakuti tsopano mukhala mamwemo;
Muona coopsa, mucitapo mantha.
22Ngati ndinati, Mundipatse?
Kapena, Muperekeko kwa ine cuma canu?
23Kapena, Mundilanditse m'dzanja la mdani?
Kapena, Mundiombole m'dzanja la oopsa?
24Mundilangize, ndipo ndidzakhala cete ine;
Mundizindikiritse umo ndinalakwira.
25Mau oongoka si ndiwo amphamvu?
Koma kudzudzula kwanu mudzudzula ciani?
26Kodi muyesa kudzudzula mau?
Popeza maneno a munthu wodololoka akunga mphepo.
27Indetu, mugwetsera wamasiye msampha,
Mumkumbira bwenzi lanu mbuna.
28Koma tsopano balindani, mundipenyerere;
Ndikanena bodza pamaso panu mudzalizindikira.
29Bwererani, ndikupemphani, musandiipsire mlandu;
Inde, bwereraninso, mlandu wanga ngwolungama.
30Kodi pali cosalungama palilime panga?
Ngati sindizindikira zopanda pace m'kamwa mwanga?

©The Bible Society of Malawi, 1992

1Kodi munthu alibe nkhondo kunja kuno?
Kodi masiku ace sakunga masiku a wolembedwa nchito?
2Monga kapolo woliralira mthunzi,
Monga wolembedwa nchito ayembekezera mphotho yace,
3Momwemo anandilowetsa miyezi yopanda pace.
Nandiikiratu zowawa usiku ndi usiku.
4Ndigona pansi, ndikuti,
Ndidzauka liti? koma usiku undikulira;
Ndipo ndimapalapata mpaka mbanda kuca.
5Mnofu wanga wabvala mphutsi ndi nkanambo zadothi;
Khungu langa lang'ambika, nilinyansa.
6Masiku anga afulumira koposa mphindo ya muomba,
Apitirira opanda ciyembekezo.
7Kumbukila kuti moyo wanga ndiwo mphepo,
Diso langa silidzaonanso cokoma.
8Diso la amene andiona silidzandionanso,
Maso ako adzandipenyetsetsa, koma ine palibe.
9Mtambo wapita watha,
Momwemo wakutsikira kumanda sadzakwerakonso.
10Sadzabweranso ku nyumba yace,
Osamdziwanso malo ace.
11Potero sindidzaletsa pakamwa panga;
Ndidzalankhula popsinjika mumzimu mwanga;
Ndidzadandaula pakuwawa mtima wanga.
12Ndine nyanja kodi, kapena cinjoka ca m'nyanja,
Kuti Inu mundiikira odikira?
13Ndikati, Pakama panga mpondisangalatsa,
Pogona panga padzacepsa condidandaulitsa;
14Pamenepo mundiopsa ndi maloto,
Nimundicititsa mantha ndi masomphenya;
15Potero moyo wanga usankha kupotedwa,
Ndi imfa, koposa mafupa anga awa.
16Ndinyansidwa nao moyo wanga; sindidzakhala ndi moyo cikhalire;
Mundileke; pakuti masiku anga ndi acabe.
17Munthu ndani kuti mumkuze,
Ndi kuti muike mtima wanu pa iye,
18Ndi kuti muceze naye m'mawa ndi m'mawa,
Ndi kumuyesa nthawi zonse?
19Mukana kundicokera kufikira liti,
Kapena kundileka mpaka nditameza dobvu?
20Ngati ndacimwa, ndingacitire Inu ciani, Inu wodikira anthu?
Mwandiikiranji ndikhale candamali canu?

Kuti ndikhale kwa ine ndekha katundu?
21Mulekeranji kukhululukira kulakwa kwanga ndi kundicotsera
mphulupulu yanga?
Popeza tsopano ndidzagona kupfumbi;
Mudzandifunafuna, koma ine palibe.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Poona tsoka lao Bilidadi akuti Yobu ndi ana ace anacimwa, anena mofanizira

1 Pamenepo anayankha Bilidadi Msuki, nati,
2 Udzanena izi kufikira liti?
Ndipo mau a pakamwa pako adzakhala ngati namondwe kufikira liti?
3 Ngati Mulungu akhotetsa ciweruzo?
Ngati Wamphamvuyonse akhotetsa mlandu?
4 Cinkana ana ako anamcimwira Iye,
Ndipo anawapereka mwa kulakwa kwao;
5 Koma ukafunitsitsa Mulungu,
Ndi kupembedza Wamphamvuyonse;
6 Ukakhala woyera ndi woongoka mtima,
Zoonadi adzakugalamukira tsopano,
Ndi kupindulitsa pokhala pako polungama.
7 Ndipo cinkana ciyambi cako cinali cacing'ono,
Citsiriziro cako cidzacuruka kwambiri.
8 Pakuti ufunsire tsono mbadwo wapitawo,
Nusamalire zimene makolo ao adazisanthula;
9 Pakuti ife ndife adzulo, osadziwa kanthu,
Popeza masiku athu a pa dziko lapansi ndiwo ngati mthunzi;
10 Amene aja sangakuphunzitse, ndi kukufotokozera,
Ndi kuturutsa mau a mumtima mwao?
11 Ngati gumbwa aphuka popanda cinyontho?
Ngati mancedza amera popanda madzi?
12 Akali auwisi, sanawaceka,
Auma, asanaume mathengo onse ena.
13 Momwemo mayendedwe a onse oiwala Mulungu;
Ndi ciyembekezo ca onyoza Mulungu cidzatayika;
14 Kulimbika mtima kwace kudzatyoka,
Cikhulupiriro cace cikunga nyumba ya tandaude.
15 Adzatsamira nyumba yace, koma yosamlimbira;
Adzaiumirira koma yosakhalitsa.
16 Akhala wamuwisi pali dzuwa,
Ndi nthambi zace ziturukira pamunda pace.
17 Mizu yace iyangayanga pa kasupe wamadzi,
Apenyerera pokhalapo miyala.
18 Akamuononga kumcotsa pamalo pace,
Padzamkana, ndi kuti, Sindinakuona.
19 Taona, ici ndico comkondweretsa panjira pace,
Ndi panthaka padzamera ena.
20 Taona, Mulungu sakana munthu wangwiro;
Kapena kugwiriziza ocita zoipa.

21Koma adzadzaza m'kamwa mwako ndi kuseka,
Ndi milomo yako kupfuula.
22Iwo akudana nawe adzabvala manyazi;
Ndi hema wa oipa adzakhala kuli zi.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Yobu abvomereza ukulu wa Mulungu, koma okoma ndi oipa alangidwa mmodzimodzi. Masautso ace amfunitsa kufa

1 Pamenepo Yobu anayankha, nati,
2 Zoona, ndidziwa kuti ciri cotero.
Koma munthu adzakhala walungama bwanji kwa Mulungu?
3 Akafuna Iye kutsutsana naye,
Sadzambwezera Iye mau amodzi onse mwa cikwi.
4 Ndiye wa mtima wanzeru, ndi wa mphamvu yaikuru;
Ndaniyo anadziumitsa mtima pa Iye, nakhala nao mtendere?
5 Ndiye amene asuntha mapiri, osacidziwa iwo,
Amene amagubuduza mu mkwiyo wace.
6 Amene agwedeza dziko lapansi licoke m'malo mwace,
Ndi mizati yace injenjemere.
7 Amene alamulira dzuwa ndipo silituruka,
Nakomera nyenyezi cizindikilo cakuzitsekera.
8 Woyala thambo yekha,
Naponda pa mafunde a panyanja.
9 Wolenga Mlalang'amba, Akamwiniatsatana, ndi Nsangwe,
Ndi Kumpotosimpita,
10 Wocita zazikuru zosasanthulika,
Ndi zodabwiza zosawerengeka,
11 Taona, Mulungu apita pali ine, koma sindimpenya;
Napitirira, koma osamaindikira ine.
12 Taona, akwatula, adzambwezetsa ndani?
Adzanena naye ndani, Mulikucita ciani?
13 Mulungu sadzabweza mkwiyo wace;
Athandizi odzikuza awerama pansi pa Iye.
14 Nanga ine tsono ndidzamyankha bwanji,
Ndi kusankha mau anga akutsutsana ndi Iye?
15 Ameneyo, cinkana ndikadakhala wolungama, sindikadamyankha;
Ndikadangompembedza wondiweruza ine.
16 Ndikadaitana, ndipo akadayankha Iye,
Koma sindikadakhulupirira kuti Iye wamvera mau anga,
17 Pakuti andityola ndi mkuntho,
Nacurukitsa mabala anga kopanda cifukwa.
18 Sandilola kuti ndipume,
Koma andidzaza ndi zowawa.
19 Tikanena za mphamvu, si ndiye wamphamvu?
Tikanena za kuweruza, adzamuitana ndani?
20 Cinkana ndikhala wolungama, pakamwa panga padzanditsutsa;
Cinkana ndikhala wangwiro, padzanditsutsa wamphulupulu.
21 Cinkana ndikhala wangwiro, sindidzisamalira mwini,
Ndipeputsa moyo wanga.

22Kuli cimodzimodzi monsemo, m'mwemo ndikuti
Iye aononga wangwiro ndi woipa pamodzi.
23Mkwapulo ukapha modzidzimutsa,
Adzaseka tsoka la wosacimwa.
24Dziko lapansi laperekedwa m'dzanja la woipa;
Aphimba maso a oweruza ace.
Ngati sindiye, pali yaninso?
25Tsopano masiku anga afulumira kuposa wamtokoma;
Athawa osaona cokoma.
26Apitirira ngati zombo zaliwiro;
Ngati mphungu igudukira cakudya cace.
27Ndikati, Ndidzaiwala condidandaulitsa,
Ndidzasintha nkhope yanga yacisoni, ndidzasekerera;
28Pamenepo ndiopa zisoni zanga zonse,
Ndidziwa kuti simudzandiyesa wosacimwa.
29Mlandu udzanditsutsa;
Potero ndigwire nchito cabe cifukwa ninji?
30Ndikasamba madzi a cipale cofewa
Ndi kuyeretsa manja anga ndi sopo;
31Mudzandibviikanso muli zoola,
Ndi zobvala zanga zidzanyansidwa nane.
32Pakuti sindiye munthu, monga ine, kuti ndimyankhe,
Kuti tikomane mlandu.
33Palibe wakutiweruza,
Wakutisanjika ife tonse awiri manja ace.
34Andicotsere ndodo yace,
Coopsa cace cisandicititse mantha;
35Kuti ndinene, osamuopa,
Pakuti sinditero monga umo ndiri.

©The Bible Society of Malawi, 1992

1Mtima wanga ulema nao moyo wanga,
Ndidzadzilolera kudandaula kwanga,
Ndidzalankhula pakuwawa mtima wanga.
2Ndidzati kwa Mulungu, Musanditsutse;
Mundidziwitse cifukwa ca kutsutsana nane.
3Cikukomerani kodi kungosautsa,
Kuti mupeputsa nchito yolemetsa manja anu,
Ndi kuti muwalira pa uphungu wa oipa?
4Muli nao maso a thupi kodi?
Mupenya kodi monga umo apenyera munthu?
5Masiku anu akunga masiku a munthu kodi,
Zaka zanu zikunga masiku a munthu;
6Kuti mufunsa mphulupulu yanga,
Ndi kulondola coipa canga;
7Cinkana mudziwa kuti sindiri woipa,
Ndipo palibe wakupulumutsa m'dzanja lanu?
8Manja anu anandiumba, nandiulunga monsemu,
Koma mufuna kundiononga.
9Mukumbukile kuti mwandiumba ngati dothi;
Ndipo kodi mudzandibwezera kupfumbi?
10Simunanditsanula kodi ngati mkaka,
Ndi kundilimbitsa ngati mase?
11Munandibveka khungu ndi mnofu,
Ndi kundilumikiza mafupa ndi mitsempha,
12Mwandipatsa moyo, ndi kundikomera mtima,
Ndi masamalidwe anu anasunga mzimu wanga.
13Koma izi munazibisa mumtima mwamu;
Ndidziwa kuti ici muli naco:
14Ndikacimwa mundipenya;
Ndipo simudzandimasula mphulupulu yanga.
15Ndikakhala woipa, tsoka ine;
Ndikakhala wolungama, sindidzakweza mutuwanga;
Ndadzazidwa ndi manyazi, Koma penyani kuzunzika kwanga.
16Ndipo mutu wanga ukadzikweza, mundisaka ngati mkango;
Mubweranso ndi kudzionetsera modabwiza kwa ine.
17Mundikonzeranso mboni zonditsutsa,
Ndi kundicurukitsira mkwiyo wanu;
Nkhondo yobwereza-bwereza yandigwera.
18Potero munandibadwitsa cifukwa ninji?
Mwenzi nditapereka moyo wanga, lisanandione diso.
19Ndikadakhala monga ngati sindikadakhala;
Akadanditenga pobadwapo kumka nane kumanda.
20Masiku anga satsala owerengeka nanga? lindani,

Bandilekani kuti nditsitsimuke pang'ono,
21Ndisanacoke kumka kumene sindikabweranso,
Ku dziko la mdima ndi la mthunzi wa imfa;
22Dziko la mdima bii ngati mdima wandiweyani,
Dziko la mthunzi wa imfa losalongosoka,
Kumene kuunika kukunga mdima.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Zofari adzudzula Yobu pa kudzilungamitsa kwace, namcenjeza alape

1 Pamenepo anayankha Zofari wa ku Naama, nati,
2 Kodi mau ocurukawa sayenera kuwayankha?
Ndi munthu wa milomo ayenera kuyesedwa wolungama?
3 Kodi zotamanda zako ziwatseke anthu pakamwa?
Useka kodi, wopanda munthu wakukucititsapo manyazi?
4 Pakuti unena, Ciphunzitso canga ncoona,
Ndipo ndiri woyera pamaso pako.
5 Koma, hal mwenzi atanena Mulungu,
Ndi kukutsegulira milomo yace motsutsa;
6 Nakufotokozere zinsinsi za nzeru,
Popeza zipindika-pindika macitidwe ao!
Cifukwa cace dziwa kuti Mulungu akuiwalira mphulupulu zina.
7 Kodi ukhoza kupeza Mulungu mwa kufunafuna?
Ukhoza kupeza Wamphamvuyonse motsindika?
8 Kumpeza kutalika ngati kumwamba, ungacitenji?
Kuzama ngati kumanda, ungadziwenji?
9 Muyeso wace utalikira utali wace wa dziko lapansi,
Citando cace ciposa ca nyanja.
10 Akapita, nakatsekera,
Nakaturutsa bwalo la mlandu, adzamletsa ndani?
11 Pakuti adziwa anthu opanda pace,
Napenyanso mphulupulu, ngakhale saisamalira.
12 Koma munthu wopanda pace asowa nzeru,
Ngakhale munthu abadwa ngati mwana wa mbidzi.
13 Ukakonzeratu mtima wako,
Ndi kumtambasulira lye manja ako;
14 Mukakhala mphulupulu m'dzanja lako, uicotseretu kutali,
Ndi cisalungamo cisakhale m'mahema mwako;
15 Popeza pamenepo udzakweza nkhope yako opanda banga;
Nudzalimbika osacita mantha;
16 Pakuti udzaiwala cisoni cako,
Udzacikumbukila ngati madzi opita;
17 Ndipo moyo wako udzayera koposa usana;
Kungakhale kuli mdima kudzakhala ngati m'mawa.
18 Ndipo udzalimbika mtima popeza pali ciyembekezo;
Nudzafunafuna, ndi kugona mosatekeseka,
19 Inde udzagona pansi, wopanda wina wakukunjenjemeretsa,
Ndipo ambiri adzakupembedza,
20 Koma maso a oipa adzagoma, Ndi pothawirapo padzawasowa,
Ndipo ciyembekezo cao ndico kupereka mzimu wao.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Yobu abvomerezanso ukulu wa Mulungu, koma mau a abwenziwo ndi opanda pace; nanena za moyo wa munthu ukutha msanga

1Pamenepo Yobu anayankha, nati,
2Zoonadi inu ndinu anthu,
Ndi nzeru idzafa pamodzi ndi inu.
3Koma inenso ndiri nayo nzeru monga inu.
Sindingakucepereni;
Ndani sadziwa zonga izi?
4Ndine ngati munthu wosekedwa ndi mnansi wace,
Ndinaitana kwa Mulungu, ndipo anandiyankha;
Munthu wolungama wangwiro asekedwa.
5Munthu wosatekeseka apeputsa tsoka mumtima mwace,
Limlindira wotererekа mapazi ace.
6Mahema a acifwamba akhala mumtendere,
Ndi iwo oputa Mulungu alimbika mtima:
Amene Mulungu amadzazira dzanja lao.
7Tafunsira tsono kwa nyamazo, zidzakulangiza,
Ndi mbalame za m'mlengalenga, zidzakuuza;
8Kapena ulankhule ndi dziko lapansi, lidzakulangiza;
Ndi nsomba za kunyanja, zidzakufotokozera,
9Ndaniyo sadziwa nazo izi zonse;
Kuti dzanja la Yehova licita ici?
10M'dzanja mwace muli mpweya wa zamoyo zonse,
Ndi mzimu wa munthu ali yense.
11M'khutumu simuyesa mau,
Monga m'kamwa mulawa cakudya cace?
12Kwa okalamba kuli nzeru,
Ndi kwa a masiku ocuruka luntha.
13Kwa Iye kuli nzeru ndi mphamvu;
Uphungu ndi luntha ali nazo.
14Taona, agamula, ndipo palibe kumanganso;
Amtsekera munthu, ndipo palibe kumtsegulira,
15Taona atsekera madzi, naphwa;
Awatsegulira, ndipo akokolola dziko lapansi.
16Kwa Iye kuli mphamvu ndi nzeru.
Wonyengedwa ndi wonyenga yemwe ali ace.
17Apita nao maphungu atawafunkhira,
Napulukiritsa oweruza milandu.
18Amasula comangira ca mafumu,
Nawamangira nsinga m'cuuno mwao.
19Apita nao, ansembe atawafunkhica,
Nagubuduza amphamvu.

20Amcotsera wokhulupirika kunena kwace.
Nalanda luntha la akulu.
21Atsanulira mnyozo pa akalonga,
Nawasezera olimba lamba lao.
22Abvumbulutsa zozama mumdima,
Naturutsa mthunzi wa imfa ukhale poyera;
23Acurukitsa amitundu, nawaononganso;
Abalalikitsa amitundu, nawabwezanso.
24Awacotsera akulu a anthu a padziko mtima wao,
Nawasokeretsa m'cipululu copanda njira.
25Iwo ayambasa mumdima mopanda kuunika,
Ndipo awayendetsa dzandi dzandi.

©The Bible Society of Malawi, 1992

1Taonani; diso langa laciona conseci;
M'khutu mwanga ndacimva ndi kucizindikira.
2Cimene mucidziwa inu, inenso ndicidziwa;
Sindikuceperani.
3Koma ine ndidzanena ndi Wamphamvuyonse,
Ndipo ndifuna kudzikanira kwa Mulungu.
4Koma inu ndinu opanga zabodza,
Asing'anga opanda pace inu nonse.
5Mwenzi mutakhala cete konse,
Ndiko kukadakhala nzeru zanu.
6Tamvani tsono kudzikanira kwanga,
Tamverani kudzinenera kwa milomo yanga.
7Kodi munenera Mulungu mosalungama,
Ndi kumnenera Iye monyenga?
8Kodi mukhalira kumodzi ndi Iye?
Mundilimbirana mwa Mulungu.
9Ncokoma kodi kuti Iye akusanthuleni?
Kodi mudzamnyenga Iye monga munyenga munthu?
10Adzakudzudzulani ndithu,
Mukacita tsankhu m'tseri.
11Ukulu wace sukucititsani mantha,
Ndi kuopsa kwace sikukugwerani kodi?
12Zikumbutso zanu ndizo miyambi ya mapulusa;
Zodzikanira zanu zikunga malinga adothi.
13Khalani cete, ndilekeni, kuti ndinene,
Condifikira cifike.
14Ndilumirenji mnofu wanga pamano panga,
Ndi kupereka moyo wanga m'dzanja langa?
15Angakhale andipha koma ndidzamlindira;
Komanso ndidzaumirira mayendedwe anga pamaso pace.
16Iye adzakhalanso cipulumutso canga,
Pakuti wonyoza Mulungu sadzafika pamaso pace.
17Mvetsetsani mau anga,
Ndi kunenetsa kwanga kumveke m'makutu mwanu.
18Taonani tsono, ndalongosola mlandu wanga;
Ndidziwa kuti adzandimasula ndiri wolungama,
19Ndaniyo adzatsutsana nane?
Ndikakhala cete, ndidzapereka mzimu wanga.
20Zinthu ziwiri zokha musandicitire,
Pamenepo sindidzabisalira nkhope yanu:
21Mundicotsere dzanja lanu kutali,
Ndi kuopsa kwanu kusandicititse mantha.
22Pamenepo muitane, ndipo ndidzayankha;

Kapena ndinene ndine, ndipo mundiyankhe ndinu.
23Mphulupulu zanga ndi zocimwa zanga ndi zingati?
Mundidziwitse kulakwa kwanga ndi cimo langa,
24Mubisiranji nkhope yanu,
Ndi kundiyesa mdani wanu?
25Kodi mudzaopsa tsamba lakungouluka,
Ndi kulondola ziputu zouma?
26Pakuti mundilembera zinthu zowawa,
Ndi kundipatsa ngati colowa mphulupulu za ubwana wanga.
27Mulonganso mapazi anga m'zigologolo, ndi kupenyerera
mayendedwe anga onse;
Mudzilembera malire mopanika mapazi anga;
28Momwemo munthu akutha ngati cinthu coola,
Ngati cobvala codyedwa ndi numbi

©The Bible Society of Malawi, 1992

Yobu 14
1Munthu wobadwa ndi mkazi
Ngwa masiku owerengeka, nakhuta mabvuto,
2Aturuka ngati duwa, nafota;
Athawa ngati mthunzi, osakhalitsa.
3Ndipo kodi mumtsegulira maso anu wotereyo,
Ndi kunditenga kunena nane mlandu Inu?
4Adzaturutsa coyera m'cinthu codetsa ndani? nnena mmodzi yense.
5Popeza masiku ace alembedwa, ciwerengo ca miyezi yace cikhala ndi Inu,
Ndipo mwamlembera malire ace, kuti asapitirirepo iye;
6Mumleke osamthira maso, kuti apumule,
Kuti akondwere nalo tsiku lace monga wolembedwa nchito.
7Pakuti akaulikha mtengo pali ciyembekezo kuti udzaphukanso,
Ndi kuti nthambi yace yanthete siidzasowa.
8Ngakhale muzu wace wakalamba m'nthaka,
Ndi tsinde lace likufa pansi;
9Koma pa mnunkho wa madzi udzaphuka,
Nudzaswa nthambi ngati womera.
10Koma munthu akufa atacita liondeonde
Inde, munthu apereka mzimu wace, ndipo ali kuti?
11Madzi acoka m'nyanja,
Ndi mtsinje ukuphwa, nuuma;
12Momwemo munthu agona pansi, osaukanso;
Kufikira miyamba kulibe, sadzaukanso,
Kapena kuutsidwa pa tulo tace.
13Ha! mukadandibisa kumanda,
Mukadandisunga m'tseri, mpaka wapita mkwiyo wanu.
Mukadandiikira nthawi, ndi kundikumbukira.
14Atafa munthu, adzakhalanso ndi moyo kodi?
Ndikadayembekeza masiku onse a nkhondo yanga,
Mpaka kwafika kusandulika kwanga,
15Mukadaitana, ndipo ndikadakuyankhani;
Mukadakhumba nchito ya manja anu.
16Koma tsopano muwerenga maponda mwanga;
Kodi simuyang'anitsa cimo langa?
17Colakwa canga caikidwa m'thumba lokomedwa cizindikilo;
Ndipo mumanga pamodzi mphulupulu zanga.
18Ndipo zoonadi, likagwa phiri, latha;
Ndi thanthwe lisunthika m'malo mwace;
19Madzi anyenya miyala;
Zosefukira zao zikokolola pfumbi la nthaka;
Ndipo muononga ciyembekezo ca munthu.

20Mumlaka cilakire, napita iye;
Musintha nkhope yace, mumuuza acoke.
21Ana ace aona ulemu osadziwa iye;
Napeputsidwa, koma osazindikira za iwo.
22Koma thupi lace limuwawira yekha,
Ndi mtima wace umliritsa yekha.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Elifazi atsutsa Yobu pa kudzikuza kwace. Akuti, akuru omwe atsimikiza kuti ocimwa sakhala bwino

1 Pamenepo Elifazi wa ku Temani anayankha, nati,
2 Kodi mwini nzeru ayankhe ndi kudziwa kouluzika,
Ndi kudzaza mimba yace ndi mphepo ya kum'mawa?
3 Kodi atsutsane ndi mnzace ndi mau akusathandiza?
Kapena ndi maneno akusaphindulitsa?
4 Zedi uyesa cabe mantha,
Nucepsa cilingiriro pamaso pa Mulungu.
5 Pakuti pakamwa pako paphunzitsa mphulupulu zako,
Nusankha lilime la ocenjerera.
6 Pakamwa pako pakutsutsa, si ine ai.
Inde milomo yako ikucitira umboni wakukutsutsa.
7 Kodi ndiwe munthu woyamba kubadwa?
Kapena unayamba kulengedwa ndiwe, osati mapiri?
8 Kodi unamva uphungu wacinsinsi wa Mulungu?
Ndipo unadzikokera nzeru kodi?
9 Udziwa ciani, osacidziwa ife?
Uzindikira ciani, cosakhala mwa ife?
10 Pakati pa ife pali aimvi, ndi okalambitsa,
Akuposa atate wako masiku ao,
11 Masangalatso a Mulungu akucepera kodi?
Kapena uli naco cinsinsi kodi?
12 Mtima wako usonthokeranji nawe?
Maso ako aphethira-phethira cifukwa ninji?
13 Kuti utembenuza mzimu wako utsutsane ndi Mulungu,
Ndi kulola mau otere aturuke m'kamwa mwako.
14 Munthu nciani kuti akhale woyera,
Wobadwa ndi mkazi kuti akhale wolungama?
15 Taona, Mulungu sakhulupirira opatulika ace;
Ngakhale m'mwamba simuyera pamaso pace,
16 Koposa kotani nanga munthu wonyansa ndi wodetsa,
Wakumwa cosalungama ngati madzi.
17 Ndidzakuonetsa, undimvere;
Cimene ndinaciona, ndidzakufotokozera;
18 Cimene adacinena anzeru,
Adacilandira kwa makolo ao, osacibisa;
19 Ndiwo amene analandira okha dzikoli,
Wosapita mlendo pakati pao;
20 Munthu woipa adzipweteka masiku ace onse,
Ndi zaka zowerengeka zisingikira woopsa.
21 M'makutu mwace mumveka zoopsetsa;
Pali mtendere amfikira wakumuononga.

22Sakhulupirira kuti adzaturukamo mumdima,
Koma kuti lupanga limlindira;
23Ayendayenda ndi kufuna cakudya, nati, Ciri kuti?
Adziwa kuti lamkonzekeratu pafupi tsiku lamdima,
24Nsautso ndi cipsinjo zimcititsa mantha,
Zimlaka ngati mfumu yokonzekeratu kunkhondo;
25Pakuti amtambasula dzanja lace moyambana ndi Mulungu,
Napikisana ndi Wamphamvuyonse.
26Amthamangira Iye mwaliuma,
Ndi zikopa zace zocindikira.
27Popeza anakuta nkhope yace ndi kunenepa kwace,
Nacita mafunyenye a mafuta m'zuuno zace;
28Adzakhala m'midzi yopasuka,
M'nyumba zosakhalamo munthu,
Zoti zisandulika muunda.
29Sadzakhala wolemera, ndi cuma cace sicidzakhalitsa,
Ndi zipatso zace sizidzacuruka padziko.
30Sadzacoka mumdima;
Lawi la moto lidzaumitsa nthambi zace;
Ndipo adzacoka ndi mpumo wa m'kamwa mwace.
31Asatame zopanda pace, kudzinyenga nazo;
Pakuti zopanda pace zidzakhala combwezera cace.
32Cidzacitika isanadze nthawi yace;
Pakuti nthambi yace siidzaphuka.
33Adzayoyoka zipatso zace zosapsa ngati mpesa,
Nadzathothoka maluwa ace ngati mtengo wazitona.
34Pakuti msonkhano wa onyoza Mulungu udzakhala cumba,
Ndi moto udzapsereza mahema a olandira cokometsera mlandu.
35Aima ndi cobvuta, nabala mphulupulu,
Ndi m'mimba mwao mukonzeratu cinyengo.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Yobu atonza mabwenziwo kuti mau ao samthandiza, akana kuti sanacimwa, nadziponya kwa Mulungu. Ciyembekezo cace ndi imfa

1Pamenepo Yobu anayankha, nati,
2Ndamva zambiri zotere;
Inu nonse ndinu otonthoza mtima mondilemetsa.
3Kodi adzatha mau ouluzika?
Kapena cikuwindula nciani kuti uyankha zotere?
4Inenso ndikadanena monga inu,
Moyo wanu ukadakhala m'malo mwa moyo wanga,
Ndikadalumikizanitsa mau akutsutsana nanu,
Ndi kukupukusirani mutu wanga.
5Koma ndikadakulimbikitsani ndi m'kamwa mwanga,
Ndi citonthozo ca milomo yanga cikadatsitsa cisoni canu.
6Cinkana ndinena cisoni canga sicitsika;
Ndipo ndikaleka, cindicokera nciani?
7Koma tsopano wandilemetsa Iye;
Mwapasula msonkhano wanga wonse.
8Kundigwira kwanu, ndiko umboni wonditsutsa,
Kuonda kwanga kundiukira, kucita umboni pamaso panga.
9Iye anding'amba m'kundida kwace, nakwiya nane,
Anandikukutira mano;
Mdani wanga ananditong'olera maso ace.
10Iwo anandiyasamira pakamwa pao;
Anandiomba pama ndi kunditonza;
Asonkhana pamodzi kunditsutsa.
11Mulungu andipereka kwa osalungama,
Nandiponya m'manja a oipa.
12Ndinali mkupuma, koma anandityola;
Inde anandigwira pakhosi, nandiphwanya;
Anandiimika ndikhale candamali.
13Eni mauta ace andizinga,
Ang'amba imso zanga, osazileka;
Natsanulira pansi ndulu yanga.
14Andipasula-pasula;
Andithamangira ngati wamphamvu.
15Ndadzisokerera ciguduli ku khungu langa,
Ndipo ndaipsa mphamvu yanga m'pfumbi.
16Nkhope yanga njodetsedwa ndi kulira misozi,
Ndi pa zikope zanga pali mthunzi wa imfa;
17Pangakhale palibe ciwawa m'manja mwanga,
Ndi pemphero langa ndi loyera.
18Dziko iwe, usakwirire mwazi wanga,

Ndi kulira kwanga kusowe popumira.
19Tsopanonso, taona, mboni yanga iri kumwamba,
Ndi nkhoswe yanga ikhala m'mwamba.
20Mabwenzi anga andinyoza; Koma diso langa lilirira misozi kwa Mulungu;
21Ha! munthu akadapembedzera mnzace kwa Mulungu,
Monga munthu apembedzera mnansi wace!
22Pakuti zitafika zaka zowerengeka,
Ndidzamuka ku njira imene sindibwererako.

©The Bible Society of Malawi, 1992

1Mzimu wanga watha, masiku anga afafanizika,
Kumanda kwandikonzekeratu.
2Zoonadi, ali nane ondiseka;
Ndi diso langa liri cipenyere m'kundiwindula kwao.
3Mupatse cigwiriro tsono, mundikhalire cikole Inu nokha kwanu;
Ndani adzapangana nane kundilipirira?
4Pakuti mwabisira mtima wao nzeru;
Cifukwa cace simudzawakuza.
5Iye wakupereka mabwenzi ace kuukapolo,
M'maso mwa ana ace mudzada.
6Anandiyesanso nthanthi za anthu;
Ndipo ndakhala ngati munthu womthira malobvu pankhope pace.
7M'diso mwanga mucita cizirezire cifukwa ca cisoni,
Ndi ziwalo zanga zonse ziribe cithunzi.
8Anthu oongoka mtima adzadabwa naco,
Ndi munthu wosalakwa adzadziutsa kumtsotsa wonyoza Mulunguyo.
9Koma wolungama asungitsa njira yace,
Ndi iye wa manja oyera adzakulabe mumphamvu.
10Koma bwerani inu nonse, idzani tsono;
Pakuti sindipeza mwa inu wanzeru.
11Masiku anga apitirira, zolingirira zanga zaduka,
Zace zace zomwe za mtima wanga.
12Zisanduliza usiku ukhale usana;
Kuunika kuyandikana ndi mdima.
13Ndikayembekezera kumanda kukhale nyumba yanga;
Ndikayala pogona panga mumdima.
14Ndikati kwa dzenje, Ndiwe atate wanga;
Kwa mphutsi, Ndiwe mai wanga ndi mlongo wanga;
15Ciri kuti ciyembekezo canga?
Inde, ciyembekezo canga adzaciona ndani?
16Cidzatsikira ku mipingiridzo ya kumanda,
Pamene tipumulira pamodzi kupfumbi.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Bilidadi atsutsa Yobu pa kudzikuza kwace, nanena za tsoka la oipa

1Pamenepo Bilidadi wa ku Suki anayankha, nati,
2Musaka mau kufikira liti?
Zindikirani, ndi pamenepo tidzanena.
3Tiyesedwa bwanji ngati nyama za kuthengo,
Ndi kukhala odetsedwa pamaso panu?
4Iwe wodzing'amba mumkwiyo mwako,
Kodi dziko lapansi lisiyidwe cifukwa ca iwe?
Kapena thanthwe lisunthike m'malo mwace?
5Inde, kuunika kwa woipa kudzazima,
Ndi lawi la moto wace silidzawala.
6Kuunikaku kudzada m'hema mwace,
Ndi nyali yace ya pamwamba pace idzazima.
7Mapondedwe ace amphamvu adzasautsidwa,
Ndi uphungu wace wace udzamgwetsa.
8Pakuti aponyedwa m'ukonde ndi mapazi ace,
Namaponda pamatanda.
9Msampha udzamgwira kucitende,
Ndi khwekhwe lidzamkola.
10Msampha woponda umbisikira pansi,
Ndi msampha wa cipeto panjira.
11Zoopetsa zidzamcititsa mantha monsemo,
Nadzampitikitsa kumbuyo kwace.
12Njala idzatha mphamvu yace,
Ndi tsoka lidzamkonzekeratu pambali pace.
13Zidzatha ziwalo za thupi lace,
Mwana woyamba wa imfa adzatha ziwalo zace.
14Adzazulidwa kuhema kwace kumene anakhulupirira;
Nadzatengedwa kumka naye kwa mfumu ya zoopsa.
15Adzakhala m'hema mwace iwo amene sali ace;
Miyala yasulfure idzawazika pokhala pace.
16Mizu yace idzauma pansi,
Ndi nthambi yace idzafota m'mwamba.
17Cikumbukilo cace cidzatayika m'dziko,
Ndipo adzasowa dzina kukhwalala.
18Adzamkankha acoke ku kuunika alowe kumdima;
Adzampitikitsa acoke m'dziko lokhalamo anthu.
19Sadzakhala naye mwana kapena cidzukulu mwa anthu amtundu wace,
Kapena wina wotsalira kumene anakhalako.
20Akudza m'mbuyo adzadabwa nalo tsiku lace,
Monga aja omtsogolera anagwidwa mantha.

21Zoonadi, zokhalamo osalungama zitero,
Ndi malo a iye amene sadziwa Mulungu ndi awa.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Yobu achulira mabwenzi ace matsoka ace, napempha amcitire cifundo, Adzitonthoza ndi Mpulumutsi wace

1Koma Yobu anayankha, nati,
2Mudzasautsa moyo wanga kufikira liti,
Ndi kundityolatyola nao mau?
3Kakumi aka mwandicititsa manyazi;
Mulibe manyazi kuti mundiumira mtima.
4Ndipo ngati ndalakwa ndithu,
Kulakwa kwanga kuli ndi ine ndekha.
5Ngati inu mudzikuza ndithu pa ine,
Ndi kundichulira mtonzo wanga kuti munditsutse nao;
6Dziwani tsopano kuti Mulungu wandikhotetsera mlandu wanga,
Nandizinga ndi ukonde wace.
7Taonani, ndipfuula kuti, Ciwawa! koma sandimvera;
Ndikuwa, koma palibe ciweruzo.
8Iye ananditsekera njira kuti ndisapitireko,
Naika mdima poyendapo ine.
9Anandibvula ulemerero wanga,
Nandicotsera korona pamutu panga,
10Nandigamula ponsepo, ndipo ndamukatu;
Nacizula ciyembekezo canga ngati mtengo.
11Wandiyatsiranso mkwiyo wace,
Nandiyesera ngati wina wa adani ace.
12Ankhondo ace andidzera pamodzi, nandiundira njira yao,
Nandimangira misasa pozinga hema wanga.
13Iye anandicotsera abale anga kutali,
Ndi odziwana nane andiyesa mlendo konse.
14Anansi anga andisowa,
Ndi odziwana nane bwino andiiwala.
15Iwo a m'nyumba mwanga ndi adzakazi anga andiyesa mlendo;
Ndine wacilendo pamaso pao.
16Ndikaitana kapolo wanga, sandibwezera mau,
Cinkana ndimpembedza pakamwa panga.
17Mpweya wanga unyansira mkazi wanga,
Cinkana ndinampembedza ndi kuchula ana a thupi langa.
18Angakhale ana ang'ono andipeputsa,
Ndikanyamuka, andinena;
19Mabwenzi anga eni eni onse anyansidwa nane;
Ndi onse ndakondana nao asandulika adani anga.
20Pfupa langa laumirira pa khungu langa ndi mnofu wanga,
Ndipo ndapulumuka ndiri nazo nkhama za mano anga.
21Ndicitireni cifundo, ndicitireni cifundo, mabwenzi anga inu;
Pakuti dzanja la Mulungu landikhudza.

22Mundilondola bwanji ngati Mulungu,
Losakukwanirani thupi langa?
23Ha! akadalembedwa mau anga!
Ha! akadalembedwa m'buku!
24Akadawazokota pathanthwe cikhalire,
Ndi cozokotera cacitsulo ndi kuthira ntobvu!
25Koma ndidziwa kuti Mombolo wanga ali ndi moyo,
Nadzauka potsiriza papfumbi.
26Ndipo khungu langa litaonongeka,
Pamenepo wopanda thupi langa, ndidzapenya Mulungu;
27Amene ndidzampenya ndekha,
Ndi maso anga adzamuona, si wina ai.
Imso zanga zatha m'kati mwanga.
28Mukati, Tiyeni timlondole!
Popeza cifukwa ca mlandu capezeka mwa ine;
29Mucite nalo mantha lupanga; Pakuti mkwiyo utenga zolakwa za lupanga,
Kuti mudziwe pali ciweruzo.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Zofari afotokozera masautso amene Mulungu atumizira oipa

1Pamenepo anayankha Zofari Mnaama, nati,
2M'mwemo zolingirira zanga zindiyankha,
Cifukwa cace ndifulumidwa m'kati mwanga.
3Ndamva kudzudzula kwakundicititsa manyazi,
Ndi mzimu wa nzeru yanga undiyankha.
4Kodi sucidziwa ici ciyambire kale lomwe,
Kuyambira anaika munthu pa dziko lapansi,
5Kuti kupfuula kokondwera kwa woipa sikukhalira kutha,
Ndi cimwemwe ca wonyoza Mulungu cikhala kamphindi?
6Cinkana ukulu wace ukwera kumka kuthambo,
Nugunda pamitambo mutu wace;
7Koma adzatayika kosatha ngati zonyansa zace;
Iwo amene adamuona adzati, Ali kuti iye?
8Adzauluka ngati loto, osapezekanso;
Nadzaingidwa ngati masomphenya a usiku.
9Diso lidamuonalo silidzamuonanso;
Ndi malo ace sadzampenyanso.
10Ana ace adzapempha aumphawi awakomere mtima;
Ndi manja ace adzabweza cuma cace.
11Mafupa ace adzala nao unyamata wace,
Koma udzagona naye pansi m'pfumbi.
12Cinkana coipa cizuna m'kamwa mwace,
Cinkana acibisa pansi pa lilime lace;
13Cinkana acisunga, osacileka,
Naoikhalitsa m'kamwa mwace;
14Koma cakudya cace cidzasandulika m'matumbo mwace,
Cidzakhala ndulu ya mphiri mkati mwace.
15Anacimeza cuma koma adzacisanzanso;
Mulungu adzaciturutsa m'mimba mwace.
16Adzayamwa ndulu ya mphiri;
Pakamwa pa njoka padzamupha.
17Sadzapenyerera timitsinje,
Toyenda nao uci ndi mafuta.
18Cimene adagwiriraco nchito, adzacibweza, osacimeza;
Sadzakondwera monga mwa zolemera zace adaziona.
19Pakuti anapsinja, nasiya aumphawi;
Analanda nyumba mwaciwawa, imene sanaimanga.
20Popeza sanadziwa kupumula m'kati mwace,
Sadzalanditsa kanthu ka zofunika zace.
21Sikunatsalira kanthu kosadya iye,
Cifukwa cace zokoma zace sizidzakhalitsa.
22Pomkwanira kudzala kwace adzakhala m'kusauka;

Dzanja la yense wobvutika lidzamgwera,
23Poti adzaze mimba yace,
Mulungu adzamponyera mkwiyo wace waukali,
Nadzambvumbitsira uwu pakudya iye.
24Adzathawa cida cacitsulo,
Ndi mubvi wa uta wamkuwa udzampyoza.
25Auzula, nuturuka m'thupi mwace;
Inde nsonga yonyezimira ituruka m'ndulu mwace;
Zamgwera zoopsa.
26Zamdima zonse zimsungikira zikhale cuma cace,
Moto wosaukoleza munthu udzampsereza;
Udzatha wotsalira m'hema mwace.
27M'mwamba mudzabvumbulutsa mphulupulu yace,
Ndi dziko lapansi lidzamuukira.
28Phindu la m'nyumba mwace lidzacoka,
Akatundu ace adzamthawa tsiku la mkwiyo wace.
29Ili ndi gawo la munthu woipa, locokera kwa Mulungu,
Ndi colowa amuikiratu Mulungu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Yobu ayankha kuti oipa ambiri amalemerera. Zooneka m'maso sizitiuza za mtima wa Mulungu

1 Pamenepo Yobu anayankha, nati,
2 Mvetsetsani mau anga;
Ndi ici cikhale citonthozo canu.
3 Mundilole, ndinene nanenso; Ndipo nditanena ine, sekani.
4 Kodi ine, kudandaula kwanga, ndidandaulira munthu?
Ndipo ndilekerenji kupsa mtima?
5 Ndiyang'anireni, nimusumwe,
Gwirani pakamwa panu.
6 Ndikangokumbukila ndibvutika mtima,
Ndi thupi langa licita nyau nyau.
7 Oipa akhaliranji ndi moyo,
Nakalamba, nalemera kwakukuru?
8 Mbeu zao zikhazikika pamodzi nao pankhope pao,
Ndi ana ao pamaso pao,
9 Nyumba zao sizitekeseka ndi mantha,
Ngakhale ndodo ya Mulungu siiwakhalira.
10 Ng'ombe yao yamphongo imakwera, yosakanika;
Ng'ombe yao yaikazi imaswa, yosapoloza.
11 Aturutsa makanda ao ngati gulu,
Ndi ana ao amabvinabvina.
12 Ayimbira lingaka ndi zeze,
Nakondwera pomveka citoliro.
13 Atsekereza masiku ao ndi zokoma,
Natsikira m'kamphindi kumanda.
14 Koma adati kwa Mulungu, Ticokereni;
Pakuti sitifuna kudziwa njira zanu.
15 Wamphamvuyonse ndiye yani kuti timtumikire?
Ndipo tidzapindulanji pakumpemphera Iye?
16 Taonani, zokoma zao siziri m'dzanja lao;
(Koma uphungu wa oipa unditalikira.)
17 Ngati nyali za oipa zizimidwa kawiri kawiri?
Ngati tsoka lao liwagwera?
Ngati Mulungu awagawira zowawa mu mkwiyo wace?
18 Ngati akunga ziputu zomka ndi mphepo,
Ngati mungu wouluzika ndi nkuntho?
19 Mukuti, Mulungu asungira ana ace a munthu coipa cace,
Ambwezere munthuyo kuti acidziwe.
20 Aone yekha cionongeko cace m'maso mwace,
Namwe mkwiyo wa Wamphamvuyonse.
21 Pakuti comsamalitsa nyumba yace nciani, atapita iye,
Ciwerengo ca miyezi yace citadulidwa pakati?

22Ngati pali munthu wakumphunzitsa Mulungu nzeru?
Popeza lye aweruza mlandu iwo okwezeka.
23Wina akufa, wabiriwiri,
Ali cikhalire ndi cipumulire.
24Mbale zace zidzala ndi mkaka;
Ndi wongo wa m'mafupa ace uli momwe.
25Koma mnzace akufa ali nao mtima wakuwawa,
Osalawa cokoma konse.
26Iwo agona cimodzimodzi kupfumbi,
Ndi mphutsi ziwakuta.
27Taonani, ndidziwa maganizo anu,
Ndi ciwembu mundilingirira moipa,
28Pakuti munena, Iri kuti nyumba ya kalonga?
Ndi hema wokhalamo woipa ali kuti?
29Simunawafunsa kodi opita m'njira?
Ndipo simusamalira zotsimikiza zao?
30Zakuti munthu woipa asungika tsiku la tsoka?
Naturutsidwa tsiku la mkwiyo?
31Adzamfotokozera ndani njira yace pamaso pace?
Nadzamlipitsa ndani pa ici anacicita?
32Potsiriza pace adzapita naye kumanda,
Nadzadikira pamanda pace,
33Zibuma za kucigwa zidzamkomera.
Adzakoka anthu onse amtsate,
Monga anamtsogolera osawerengeka.
34Potero munditonthozeranji nazo zopanda pace,
Popeza m'mayankho mwanu mutsala mabodza okha?

©The Bible Society of Malawi, 1992

Elifazi amchulira Yobu zoipa zambiri, namuuza alape, Mulungu nadzamcitira cifundo

1 Pamenepo Elifazi wa ku Temani anayankha, nati,
2 Kodi munthu apindulira Mulungu?
Koma wanzeru angodzipindulira yekha.
3 Kodi Wamphamvuyonse akondwera nako kuti iwe ndiwe wolungama?
Kapena kodi apindula nako kuti ukwaniritsa njira zako?
4 Kodi akudzudzula, nadza nawe kumlandu,
Cifukwa ca kumuopa kwako?
5 Zoipa zako sizicuruka kodi?
Ndi mphulupulu zako sizikhala zosawerengeka kodi?
6 Pakuti wamtenga cikole kwa mbale wako wopanda cifukwa,
Ndi kubvula ausiwa zobvala zao.
7 Sunampatsa wolema madzi amwe,
Ndi wanjala unammana cakudya.
8 Koma munthu mwini mphamvu, dziko ndi lace;
Ndi munthu wobvomerezeka, anakhala momwemo.
9 Unabweza akazi amasiye osawaninkha kanthu,
Ndi manja a ana amasiye anatyoledwa.
10 Cifukwa cace misampha ikuzinga.
Ndi mantha akubvuta modzidzimutsa,
11 Kapena mdima kuti ungaone,
Ndi madzi aunyinji akumiza.
12 Kodi Mulungu sakhala m'mwamba m'tali?
Ndipo penyani kutalika kwace kwa nyenyezi, ziri m'talitali.
13 Ndipo ukuti, Adziwa ciani Mulungu?
Aweruza kodi mwa mdima wa bii?
14 Mitambo ndiyo comphimba, kuti angaone;
Ndipo amayenda pa thambo lakumwamba.
15 Udzasunga kodi njira yakale,
Anaiponda anthu amphulupulu?
16 Amene anakwatulidwa isanafike nyengo yao,
Cigumula cinakokolola kuzika kwao;
17 Amene anati kwa Mulungu, Ticokereni;
Ndipo, Angaticitire ciani Wamphamvuyonse?
18 Angakhale Iye adadzaza nyumba zao ndi zabwino;
Koma uphungu wa oipa unditalikira.
19 Olungama aciona nakondwera; Ndi osalakwa awaseka pwepwete,
20 Ndi kuti, Zoonadi, otiukirawo alikhidwa,
Ndi zowatsalira, moto unazipsereza.
21 Uzolowerane ndi Iye, nukhale ndi mtendere;
Ukatero zokoma zidzakudzera,

22Landira tsono cilamulo pakamwa pace,
Nuwasunge maneno ace mumtimamwako.
23Ukabweranso kwa Wamphamvuyonse, udzamanga bwino;
Ukacotsera cosalungama kutali kwa mahema ako.
24Ndipo utaye cuma cako kupfumbi,
Ndi golidi wa ku ofiri ku miyala ya kumitsinje.
25Ndipo Wamphamvuyonse adzakhala cuma cako,
Ndi ndarama zako zofunika.
26Pakuti pamenepo udzakondwera naye Wamphamvuyonse,
Ndi kuweramutsa nkhope yako kwa Mulungu.
27Udzampemphera ndipo adzakumvera;
Nudzatsiriza zowinda zako.
28Ukatsimikiza mtima kakuti, kadzakhazikikira iwe;
Ndi kuunika kudzawala pa njira zako.
29Anthu akakugwetsa pansi, udzati, Adzandikweza;
Ndipo adzapulumutsa wodzicepetsayo.
30Adzamasula ngakhale woparamula,
Inde adzamasuka mwa kuyera kwa manja ako.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Yobu abwereza kukana kuti sanacimwa. Mulungu wosadziwika acita cifuniro cace. Kwambiri ocimwa oyenera kulangidwa akhala bwino m'moyo uno

1Koma Yobu anayankha, nati,
2Lero lomwe kudandaula kwanga kumawawa;
Kulanga kwanga kuposa kubuula kwanga m'kulemera kwace.
3Ha! ndikadadziwa kumene ndikampeza Mulungu,
Kuti ndifike ku mpando wace!
4Ndikadalongosola mlandu wanga pamaso pace,
Ndikadadzaza m'kamwa mwanga ndi matsutsano.
5Ndikadadziwa mau akadandiyankha ine,
Ndikadazindikira cimene akadanena nane.
6Akadatsutsana nane kodi mwa mphamvu yace yaikuru?
Iai, koma akadandicherera khutu.
7Apo woongoka mtima akadatsutsana naye;
Ndipo ndikadapulumuka cipulumukire kwa Woweruza wanga.
8Taonani, ndikamka m'tsogolo, kulibe Iye;
Kapena m'mbuyo sindimzindikira;
9Akacita Iye kulamanzere, sindimpenyerera;
Akabisala kulamanja, sindimuona,
10Koma adziwa njira ndilowayi;
Atandiyesa ndidzaturuka ngati golidi.
11Phazi langa lagwiratu moponda Iye,
Ndasunga njira yace, wosapambukamo.
12Sindinabwerera kusiya malamulo a pa milomo yace;
Ndasungitsa mau a pakamwa pace koposa lamulo langa langa.
13Koma Iye ndiye wa mtima umodzi, adzambweza ndani?
Ndi ici cimene moyo wace ucifuna acicita.
14Pakuti adzacita condiikidwiratu;
Ndipo zambiri zotere ziri ndi Iye.
15Cifukwa cace ndiopsedwa pankhope pace;
Ndikalingirira, ndicita mantha ndi Iye.
16Pakuti Mulungu walefula mtima wanga,
Ndi Wamphamvuyonse wandiopsa.
17Popeza sindinalikhidwa usanafike mdimawo,
Ndipo sanandiphimbira nkhope yanga ndi mdima wa bii.

©The Bible Society of Malawi, 1992

1Wamphamvuyonse alekeranji kuikiratu nyengo?
Ndi iwo omdziwa alekeranji kudziwa masiku ace?
2Alipo akusendeza malire;
Alanda gulu la zoweta, nazidyetsa.
3Akankhizira kwao buru wa amasiye,
Atenga ng'ombe ya mfedwa ikhale cikole.
4Apambukitsa aumphawi m'njira;
Osauka a padziko abisala pamodzi.
5Taonani, ngati mbidzi za m'cipululu
Aturukira ku nchito zao, nalawirira nkufuna cakudya;
Cipululu ciwaonetsera cakudya ca ana ao.
6Atema dzinthu zao m'munda;
Natola khunkha m'munda wampesa wa woipa.
7Agona amarisece usiku wonse opanda cobvala,
Alibe copfunda pacisanu.
8Abvumbwa ndi mvula kumapiri,
Nafukata thanthwe posowa pousapo.
9Akwatula wamasiye kubere,
Natenga cikole cobvala ca osauka;
10Momwemo ayenda amarisece opanda cobvala,
Nasenza mtolo wa dzinthu ali ndi njala.
11M'kati mwa malinga a iwo aja ayenga mafuta;
Aponda mphesa moponderamo, namva ludzu.
12M'mudzi waukuru anthu abuula alinkufa;
Ndi moyo wa iwo olasidwa upfuula;
Koma Mulungu sasamalira coipaco.
13Iwo ndiwo amene apikisana nako kuunika,
Sadziwa njira zace,
Sasunga mayendedwe ace.
14Kukaca auka wambanda, napha wosauka ndi waumphawi;
Ndi usiku asanduka mbala.
15Ndipo diso la wacigololo liyombekezera cisisira,
Ndi kuti, Palibe diso lidzandiona;
Nabvala cophimba pankhope pace.
16Kuli mdima aboola nyumba,
Usana adzitsekera,
Osadziwa kuunika.
17Pakuti iwo onse auyesa m'mawa mthunzi wa imfa;
Pakuti adziwa zoopsa za mthunzi wa imfa.
18Atengedwa ngati coyandama pamadzi;
Gawo lao litembereredwa padziko;
Sadzalunjikanso njira ya minda yamphesa.
19Cirala ndi dzuwa zitha madzi a cipale cofewa,

Momwemo manda acita nao ocimwa.
20M'mimba mudzamuiwala; mphutsi zidzamudya mokondwera.
Sadzamkumbukilanso;
Ndipo cosalungama cidzatyoledwa ngati mtengo.
21Alusira cumba wosabala,
Osamcitira wamasiye cokoma.
22Mulungu awakhalitsa amphamvu mwa mphamvu yace;
Iwo aukanso m'mene anayesa kuti sadzakhala ndi moyo.
23Awalola akhale osatekeseka, ndipo alimbikapo;
Koma maso ace ali pa njira zao.
24Akwezeka; m'kamphindi kuti zi;
Inde atsitsidwa, acotsedwa monga onse ena,
Adutidwa ngati tirigu ngala zace.
25Ndipo ngati si kutero, anditsutsa ndani kuti ndiri wabodza,
Ndi kuyesa mau anga opanda pace?

©The Bible Society of Malawi, 1992

Bilidadi akuti munthu sayenera kudziyesa wolungama pamaso pa Mulungu

1Pamenepo Bilidadi wa ku Suki anayankha, nati,
2Kulamulira ndi kuopsa kuti ndi Iye;
Acita mtendere pa zam'mwamba zace.
3Ngati awerengedwa makamu ace?
Ndipo ndaniyo, kuunika kwace sikumturukira?
4Potero munthu akhala bwanji wolungama kwa Mulungu?
Kapena wobadwa ndi mkazi akhala woyera bwanji?
5Taonani, ngakhale mwezi ulibe kuwala;
Ndi nyenyezi siziyera pamaso pace;
6Kopambana kotani nanga munthu, ndiye mphutsi!
Ndi wobadwa ndi munthu, ndiyo nyongolotsi!

©The Bible Society of Malawi, 1992

Yobu atsutsa Bilidadi kuti sanamthandiza; yekha nalemekeza ukulu wa Mulungu

1Koma Yobu anayankha, nati,
2Wamthandiza bwanji wopanda mphamvu,
Kulipulumutsa dzanja losalimba!
3Wampangira bwanji wopanda nzeruyu!
Ndi kudziwitsa nzeru zeni zeni mocurukal
4Wafotokozera yani mau?
Ndi mzimu wa yani unaturuka mwa iwe?
5Adafawo anjenjemera
Pansi pa madzi ndi zokhalamo,
6Kumanda kuli padagu pamaso pace,
Ndi kucionongeko kusowa cophimbako,
7Ayala kumpoto popanda kanthu, Nalenjeka dziko pacabe.
8Amanga madzi m'mitambo yace yocindikira;
Ndi mtambo sung'ambika pansi pace,
9Acingira pa mpando wace wacifumu,
Nayalapo mtambo wace.
10Analembera madziwo malire,
Mpaka polekeza kuunika ndi mdima.
11Mizati ya thambo injenjemera,
Ndi kudabwa pa kudzudzula kwace.
12Mwa mphamvu yace agwetsa nyanja bata;
Ndipo mwa luntha lace akantha kudzikuza kwace.
13Mwa mzimu wace anyezimiritsa thambo;
Dzanja lace linapyoza njoka yothawayo.
14Taonani, awa ndi malekezero a njira zace;
Ndi cimene tikumva za Iye ndi cinong'onezo cacing'ono;
Koma kugunda kwa mphamvu yace akuzindikiritsa ndani?

©The Bible Society of Malawi, 1992

Yobu adzikaniza nanenetsa kuti ocimwa ambiri akhala osalangidwa. Ena ali ndi nzeru ndi cuma, koma opanda nzeru yeni yeni

1Ndipo Yobu anaonjezanso mwambi wace, nati,
2Pali Mulungu, amene anandicotsera zoyenera ine,
Ndi Wamphamvuyonse, amene anawawitsa moyo wanga,
3Pakuti moyo wanga wonse ukali mwa ine,
Ndi mpweya wa Mulungu m'mphuno mwanga;
4Milomo yanga siilankhula cosalungama,
Ndi lilime langa silichula zacinyengo.
5Sindibvomereza konse kuti muli olungama;
Mpaka kufa ine sinditaya ungwiro wanga.
6Ndiumirira cilungamo canga, osacileka;
Cikhalire moyo ine, mtima wanga sunditonza.
7Mdani wanga akhale ngati woipa,
Ndi iye amene andiukira ngati wosalungama.
8Pakuti ciyembekezo ca wonyoza Mulungu nciani pomlikhatu Mulungu,
Pomcotsera moyo wace?
9Kodi Mulungu adzamvera kupfuula kwace, ikamdzera nsautso?
10Kodi adzadzikondweretsa naze Wamphamvuyonse,
Ndi kuitana kwa Mulungu nthawi zonse?
11Ndidzakulangizani za dzanja la Mulungu;
Cokhala ndi Wamphamvuyonse sindidzacibisa.
12Taonani, inu nonse munaciona;
Ndipo mugwidwa nazo zopanda pace cifukwa ninji?
13Ili ndi gawo la munthu woipa kwa Mulungu,
Ndi colowa ca akupsinja anzao acilandira kwa Wamphamvtiyonse.
14Akacuruka ana ace, ndiko kucurukira lupanga,
Ndi ana ace sadzakhuta cakudya. 15Akumtsalira iye adzaikidwa muimfa,
Ndi akazi ace amasiye sadzalira maliro.
16Cinkana akundika ndalama ngati pfumbi,
Ndi kukonzeratu zobvala ngati dothi;
17Azikonzeretu, koma wolungama adzazibvala,
Ndi wosalakwa adzagawa ndalamazo.
18Amanga nyumba yace ngati kadzoce,
Ndi ngati wolindira amanga dindiro.
19Agona pansi ali wacuma, koma saikidwa;
Potsegula maso ace, wafa cikomo,
20Zoopsa zimgwera ngati madzi;
Nkuntho umtenga usiku.
21Mphepo ya kum'mawa Imtenga, nacokaiye;

Nimkankha acoke m'malo mwace.
22Pakuti Mulungu adzamponyera zoopsa, osanlieka;
Kuthawa akadathawa m'dzanja lace.
23Anthu adzamuombera manja,
Nadzamuyimbira mluzu acoke m'malo mwace.

©The Bible Society of Malawi, 1992

1Koma kuli mtapo wa siliva, Ndi malo a golidi amene amuyenga.
2Citsulo acitenga m'nthaka,
Ndi mkuwa ausungunula kumwala.
3Munthu athawitsa mdima,
Nafunafuna mpaka malekezero onse,
Miyala ya mdima wa bii ndi ya mthunzi wa imfa.
4Aboola mgodi posiyana patali pokhala anthu;
Aiwalika ndi phazi lopitapo;
Apacikika kutali ndi anthu, nalendewa-lendewa.
5Kunena za nthaka, kucokera momwemo mumaturuka cakudya,
Ndi m'munsi mwace musandulizika ngati ndi moto.
6Miyala yace ndiyo malo a safiro,
Ndipo iri nalo pfumbi lagolidi.
7Njira imeneyi palibe ciombankhanga ciidziwa;
Lingakhale diso la kabawi losapenyapo.
8Nyama zodzikuza sizinapondapo,
Ngakhale mkango waukali sunapitapo.
9Munthu atambasulira dzanja lace kumwala;
Agubuduza mapiri kuyambira kumizu.
10Asema njira pakati pa matanthwe,
Ndi diso lace liona ciri conse ca mtengo wace.
11Atseka mitsinje ingadonthe;
Naturutsira poyera cobisikaci.
12Koma nzeru, idzapezeka kuti?
Ndi luntha, malo ace ali kuti?
13Munthu sadziwa mtengo wace;
Ndipo silipezeka m'dziko la amoyo.
14Pozama pakuti, Mwa ine mulibe;
Ndi nyanja ikuti, Kwa ine kulibe.
15Silipezeka ndi golidi,
Sayesapo siliva mtengo wace.
16Sailinganiza ndi golidi wa Ofiri,
Ndi sohamu wa mtengo wace wapatali kapena safiro.
17Golidi ndi krustalo sizilingana nayo;
Ndi kusinthana kwace, siisinthanika ndi zisambiro za golidi woyengetsa.
18Korali kapena ngale sizikumbukikapo.
Mtengo wace wa nzeru uposa wa korali wofiira.
19Topazi wa Kusi sufanana nayo,
Sailinganiza ndi golidi wolongosoka.
20Koma nzeru ifuma kuti?
Ndi luntha, pokhala pace pali kuti?
21Popeza pabisikira maso a zamoyo zonse,

Pabisikiranso mbalame za m'mlengalenga,
22Cionongeko ndi Imfa zikuti,
Tamva mbiri yace m'makutu mwathu.
23Mulungu ndiye: azindikira njira yace,
Ndiye adziwa pokhala pace.
24Pakuti apenyerera malekezero a dziko lapansi,
Naona pansi pa thambo ponse;
25Pamene anaikira mphepo muyeso wace,
Nayesera madzi miyeso;
26Pakucitira mvula lamulo,
Ndi njira yoyendamo mphezi ya bingu;
27Pamenepo anaiona nzeru, naifotokozera;
Anaikonza, naisanthula.
28Koma kwa munthu anati,
Taonani, kuopa Ambuye ndiko nzeru;
Ndi kupatukana naco coipa ndiko luntha.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Yobu alinganiza cikhalidwe cace cakale ndi tsoka latsopano, nalimbika kuti sanacita zochulidwazi

1 Ndipo Yobu anaonjezanso mwambi wace, nati,
2 Ha! ndikadakhala monga m'miyezi yapitayi,
Monga m'masiku akundisunga Mulungu;
3 Muja nyali yace inawala pamutu panga,
Ndipo ndi kuunika kwace ndinayenda mumdima;
4 Monga umo ndinakhala m'masiku anga olimba,
Muja uphungu wa Mulungu unakhala pahema panga;
5 Muja Wamphamvuyonse akali nane pamodzi,
Ndi ana anga anandizinga;
6 Muja popondera ine padakhatamira ndi mafuta amkaka,
Ndi thanthwe linanditsanulira mitsinje ya mafuta aazitona!
7 Muja ndinaturuka kumka kucipata kumudzi,
Muja ndinakonza pokhala panga kukhwalala,
8 Anyamata anandiona nabisala,
Okalamba anandinyamukira, nakhala ciriri,
9 Akalonga anadziletsa kulankhula,
Ndi kugwira pakamwa pao;
10 Mau a omveka anali zi,
Ndi lilime lao linamamatira ku malakalaka ao.
11 Pakuti pondimva ine khutu, linandidalitsa;
Ndipo pondiona diso, linandicitira umboni.
12 Pakuti ndinapulumutsa wozunzika wakupfuula;
Mwana wamasiye yemwe wosowa mthandizi.
13 Dalitso la iye akati atayike linandidzera,
Ndi mtima wa mkazi wamasiye ndinauyimbitsa mokondwera.
14 Ndinabvala cilungamo, ndipo cinandibvala ine;
Ciweruzo canga cinanga mwinjiro ndi nduwira.
15 Ndinali maso a akhungu,
Ndi mapazi a otsimphina.
16 Ndinali atate wa waumphawi;
Ndi mlandu wa iye amene sindinamdziwa ndinafunsitsa.
17 Ndipo ndinatyola nsagwada ya wosalungama,
Ndi kukwatula cogwidwa kumano kwace.
18 Pamenepo ndinati, Ndidzatsirizika m'cisa canga;
Ndipo ndidzacurukitsa masiku anga ngati mcenga.
19 Muzu wanga watambalala kufikira kumadzi;
Ndi mame adzakhala pa nthambi yanga usiku wonse.
20 Ulemu wanga udzakhala wosaguga mwa ine,
Ndi uta wanga udzakhala wosalifuka m'dzanja mwanga.
21 Anthu anandimvera, nalindira,
Nakhala cete, kuti ndiwapangire.

22Nditanena mau anga sanalankhulanso,
Ndi kunena kwanga kunawakhera.
23Anandilindira ngati kulindira mvula,
Nayasama pakamwa pao ngati kulira mvula ya masika.
24Ndinawaseka akapanda kulimbika mtima;
Ndipo sanagwetsa kusangalala kwa nkhope yanga.
25Ndinawasankhira njira yao ndi kukhala mkuru wao.
Ndinakhala ngati mfumu mwa ankhondo ace,
Ngati wotonthoza ofedwa.

©The Bible Society of Malawi, 1992

1Koma tsopano iwo osafikana msinkhu wanga andiseka,
Iwo amene atate ao ndikadawapeputsa, osawaika pamodzi ndi agaru olinda nkhosa zanga.
2Mphamvunso ya m'manja mwao ndikadapindulanji nayo?
Ndiwo anthu amene unyamata wao udatha,
3Atsala mafupa okha okha ndi kusowa ndi njala;
Akungudza nthaka youma kuli mdima wa m'cipululu copasuka.
4Achera terere lokolera kuzitsamba,
Ndi cakudya cao ndico mizu ya dinde.
5Anawapitikitsa pakati pa anthu,
Awapfuulira ngati kutsata mbala.
6Azikhala m'zigwa za cizirezire,
M'maenje a m'nthaka ndi m'mapanga.
7Pakati pa zitsamba alira ngati buru,
Pansi pa khwisa asonkhana pamodzi.
8Ndiwo ana a opusa, inde ana a anthu opanda dzina;
Anawaingitsa kuwacotsa m'dziko.
9Koma tsopano ndasanduka nyimbo ya oterewo,
Nandiyesa nthanthi.
10Anyansidwa nane, akhala patali ndi ine,
Saleka kuthira malobvu pankhope panga.
11Pakuti anamasula nsinga zao, nandizunza;
Anataya comangira m'kamwa mwao pamaso panga.
12Ku dzanja langa lamanja anauka oluluka,
Akankha mapazi anga,
Andiundira njira zao zakundiononga.
13Aipsa njira yanga,
Athandizana ndi tsoka langa;
Ndiwo anthu omwewo osowa mthandizi.
14Akudza ngati opitira pogamuka linga papakuru,
Pakati pa zopasuka adzigubuduza kundidzera ine.
15Anditembenuzira zondiopsa,
Auluza ulemu wanga ngati mphepo;
Ndi zosungika zanga zapita ngati mtambo.
16Ndipo tsopano moyo wanga udzitsanulira m'kati mwanga;
Masiku akuzunza andigwira.
17Nyengo ya usiku mafupa anga awaza mwa ine,
Ndi zowawa zondikungudza sizipuma.
18Mwa mphamvu yaikuru ya nthenda yanga cobvala canga cinasandulika,
Cindithina ngati pakhosi pa maraya anga.
19Iye anandiponya m'matope,
Ndipo ndafanana ndi pfumbi ndi phulusa.

20Ndipfuula kwa Inu, koma simundiyankha;
Ndinyamuka, ndipo mungondipenyerera.
21Mwasandulika kundicitira nkharwe;
Ndi mphamvu ya dzanja lanu mundizunza.
22Mundikweza kumphepo, mundiyendetsa pomwepo;
Ndipo mundisungunula mumkuntho.
23Pakuti ndidziwa kuti mudzandifikitsa kuimfa,
Ndi ku nyumba yokomanamo amoyo onse.
24Koma munthu akati agwe, satambasula dzanja lace kodi?
Akati aonongeke, sapfuulako kodi?
25Kodi sindinamlirira misozi wakulawa zowawa?
Kodi moyo wanga sunacitira cisoni osowa?
26Muja ndinayembekeza cokoma cinadza coipa,
Ndipo polindira kuunika unadza mdima.
27M'kati mwanga mupweteka mosapuma,
Masiku a mazunzo andidzera.
28Ndiyenda ndiri wothimbirira osati ndi dzuwa ai;
Ndinyamuka mumsonkhano ndi kupfuula,
29Ndiri mbale wao wa ankhandwe,
Ndi mnansi wao wa nthiwatiwa.
30Khungu langa lada, nilindipfundukira;
Ndi mafupa anga awawa ndi kutentha kwao.
31Cifukwa cace zeze wanga wasandulika wa maliro,
Ndi citoliro canga ca mau a olira misozi.

©The Bible Society of Malawi, 1992

1Ndinapangana ndi maso anga,
Potero ndipenyerenji namwali?
2Pakuti gawo la Mulungu locokera kumwamba,
Ndi colowa ca Wamphamvuyonse cocokera m'mwambamo nciani?
3Si ndizo cionongeko ca wosalungama,
Ndi tsoka la ocita mphulupulu?
4Nanga sapenyanjira zanga,
Ndi kuwerenga moponda mwanga monse?
5Ngati ndinayanjana nalo bodza,
Ndi phazi langa linathamangira cinyengo;
6Andiyese ndi muyeso wolingana,
Kuti Mulungu adziwe ungwiro wanga.
7Ngati phazi langa linapambuka m'njira,
Ndi mtima wanga unatsata maso anga?
Ngati cirema camamatira manja anga?
8Ndibzale ine nadye wina,
Ndi zondimerera ine zizulidwe.
9Ngati mtima wanga wakopeka ndi mkazi,
Ngati ndalalira pa khomo la mnzanga,
10Mkazi wanga aperere wina;
Wina namuike kumbuyo.
11Pakuti ico ndi coipitsitsa,
Ndico mphulupulu yoyenera oweruza anene mlandu wace.
12Pakuti ndico moto wakunyeka mpaka cionongeko,
Ndi cakuzula zipatso zanga zonse.
13Ngati ndapeputsa mlandu wa kapolo wanga, kapena wa mdzakazi wanga,
Potsutsana nane iwo,
14Ndidzatani ponyamuka Mulungu?
Ndipo pondizonda Iye ndidzamyankha ciani?
15Kodi Iye amene anandilenga ine m'mimba sanamlenga iyenso?
Sindiye mmodzi anatiumba m'mimba?
16Ngati ndakaniza aumphawi cifuniro cao,
Kapena kutopetsa maso a amasiye,
17Kapena kudya nthongo yanga ndekha,
Osadyako mwana wamasiye;
18(Pakuti kuyambira ubwana wanga analeredwa ndi ine monga ndi atate;
Ndipo ndinakhala nkhoswe ya wamasiye cibadwire ine.)
19Ngati ndinaona wina alinkutayika wopanda cobvala,
Kapena kuti wosowa alibe copfunda;
20Ngati zuuno zace sizinandiyamika,
Ngati sanapfunda ubweya wa nkhosa zanga;

21Ngati ndinasamulira ana amasiye dzanja langa,
Popeza ndinaona thandizo langa kucipata;
22Libanthuke phewa langa paphalo,
Ndi dzanja langa liduke pagwangwa.
23Pakuti tsoka locokera kwa Mulungu linandiopsa,
Ndi cifukwa ca ukulu wace sindinakhoza kanthu,
24Ngati ndayesa golidi ciyembekezo canga,
Ndi kunena ndi golidi woyengetsa,
Ndiwe cikhazikitso canga;
25Ngati ndinakondwera popeza cuma canga ncacikuru,
Ndi dzanja langa lapeza zocuruka;
26Ngati ndalambira dzuwa lirikuwala,
Kapena mwezi ulikuyenda monyezimira;
27Ndi mtima wanga wakopeka m'tseri,
Ndi pakamwa panga padapsompsona dzanja langa;
28Icinso ndi mphulupulu yoyenera oweruza kunena mlandu wace;
Pakuti ndikadakana Mulungu ali m'mwamba.
29Ngati ndakondwera nalo tsoka la wondida,
Kapena kudzitukula pompeza coipa;
30Ndithu sindinalola m'kamwa mwanga mucimwe,
Kupempha motemberera moyo wace.
31Ngati amuna a m'hema mwanga sanati,
Ndani adzapeza munthu wosakhuta nyama yomgawira Yobu?
32Mlendo sakagona pakhwalala,
Koma ndinatsegulira wam'njira pakhomo panga.
33Ngati ndakwirira zolakwa zanga monga Adamu,
Ndi kubisa mphulupulu yanga m'cifuwa mwanga;
34Popeza ndinaopa unyinji waukuru,
Ndi cipepulo ca mapfuko cinandiopsetsa;
Potero ndinakhala cete osaturuka pakhomo panga.
35Ha! ndikadakhala naye wina wakundimvera,
Cizindikilo canga sici, Wamphamvuyonse andiyankhe;
Mwenzi ntakhala nao mau akundineneza analemberawo mdani wangal
36Ndithu ndikadawasenza paphewa panga,
Ndi kudzimangirira awa ngati korona.
37Ndikadamfotokozera ciwerengo ca mopondamo mwanga,
Ndikadamsenderera Iye ngati ka longa,
38Ngati minda yanga ipfuula monditsutsa,
Ndi nthumbira zace zilira pamodzi;
39Ngati ndadya zipatso zace wopanda ndarama,
Kapena kutayitsa eni ace moyo wao;
40Imere minga m'malo mwa tirigu,
Ndi dawi m'malo mwa barele.

Mau a Yobu atha.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Elihu adzudzula Yobu ndi mabwenzi atatu omwe

1Pamenepo amuna atatuwa analeka kumyankha Yobu; pakuti anali
wolungama pamaso pace pa iye mwini. 2Ndipo adapsa mtima Elihu
mwana wa Barakeli wa ku Buzi, wa cibale ca Ramu, adapsa mtima
pa Yobu; pakuti anadziyesera yekha wolungama, wosati
Mulungu. 3Adapsa mtima pa mabwenzi ace atatu omwe, pakuti
anasowa pomyankha; koma anamtsutsa Yobu kuti ali woipa. 4Ndipo
Elihu analindira kulankhula ndi Yobu, popeza akulu misinkhu ndi
iwowa. 5Koma pakuona Elihu kuti anthu atatuwa anasowa
poyankha pakamwa pao anapsa mtima.
6Ndipo Elihu mwana wa Barakeli wa ku Buzi anayankha, nati,
Ine ndine mnyamata, inu ndinu okalamba;
Cifukwa cace ndinadziletsa, ndi kuopa kukuonetsani monga umo
ndayesera ine.
7Ndinati, Amisinkhu anene,
Ndi a zaka zocuruka alangize nzeru.
8Koma m'munthu muli mzimu,
Ndi mpweya wa Wamphamvuyonse wawazindikiritsa.
9Akulu sindiwo eni nzeru,
Ndi okalamba sindiwo ozindikira ciweruzo.
10Cifukwa cace ndinati, Ndimvereni ine,
Inenso ndidzaonetsa monga umo ndayesera ine.
11Taonani, ndinalindira mau anu,
Ndinacherera khutu zifukwa zanu,
Pofunafuna inu ponena.
12Inde ndinasamalira inu;
Koma taonani, panalibe womtsutsa Yobu,
Kapena wakumbwezera mau pakati painu.
13Msamati, Tapeza nzeru ndife,
Mulungu akhoza kumkhulula, si munthu ai;
14Popeza sanandiponyera ine mau,
Sindidzamyankha ndi maneno anu.
15Asumwa, sayankhanso, Anawathera mau.
16Kodi ndidzangolindira popeza sanena iwo,
Popeza akhala du osayankhanso?
17Ndidzayankha inenso mau anga,
Ndidzaonetsa inenso za m'mtima mwanga.
18Pakuti ndadzazidwa ndi mau,
Ndi mzimu wa m'kati mwanga undifulumiza.
19Taonani, m'cifuwa mwanga muli ngati vinyo wosowa popungulira,
Ngati matumba atsopano akuti aphulike.
20Ndidzanena kuti cifundo citsike;
Ndidzatsegula milomo yanga ndi kuyankha.

21Ndisati ndisamalire nkhope ya munthu,
Kapena kumchula munthu maina omdyola nao;
22Pakuti sindidziwa kuchula maina osyasyalika;
Ndikatero Mlengi wanga adzandicotsa msanga.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Elihu atsutsa Yobu pa kudzikuza kwace, nanenetsa kuti pomlanga munthu Mulungu ali naco cifukwa

1Komatu, Yobu, mumvere maneno anga,
Mucherere khutu mau anga.
2Taonani tsono, ndatsegula pakamwa panga,
Lilime langa lanena m'kamwa mwanga.
3Maneno anga aulula ciongoko ca mtima wanga,
Ndi monga umo idziwira milomo yanga idzanena zoona.
4Mzimu wa Mulungu unandilenga,
Ndi mpweya wa Wamphamvuyonse umandipatsa moyo.
5Ngati mukhoza, mundiyankhe;
Mulongosolere mau anu pamaso panga, mukonzeke.
6Taonani, ndikhala kwa Mulungu ngati inu;
Inenso ndinaumbidwa ndi dothi,
7Taonani, kuopsa kwanga simudzacita nako mantha;
Ndi ici ndikusenzetsani sicidzakulemererani.
8Zedi mwanena m'makutu mwanga,
Ndinamvanso mau akunena kwanu, akuti,
9Ndine woyera ine, wopanda kulakwa,
Ndine wosaparamula, ndiribe mphulupulu.
10Taonani, Iye apeza zifukwa zoti anditsutse nazo,
Andiyesa mdani wace;
11Amanga mapazi anga m'zigologolo,
Ayang'anira poyenda ine ponse.
12Taonani, ndidzakuyankhani m'mene muli mosalungama;
Pakuti Mulungu ndiye wamkulu woposa munthu.
13Mutsutsana ndi Iye cifukwa ninji?
Popeza pa zace zonse saulula cifukwa.
14Pakuti Mulungu alankhula kamodzi,
Kapena kawiri, koma anthu sasamalira.
15M'kulota, m'masomphenya a usiku,
Pakuwagwera anthu tulo tatikuru,
Pogona mwacheru pakama,
16Pamenepo atsegula makutu a anthu,
Nakomera cizindikilo cilangizo cao;
17Kuti acotse munthu ku cimene akadacita,
Ndi kubisira munthu kudzikuza kwace;
18Kuti amletse angaonongeke,
Ndi moyo wace ungatayike ndi lupanga.
19Alangidwanso ndi zowawa pakama pace,
Ndi kulimbana kowawa kosapuma m'mafupa ace.
20M'mwemo mtima wace ucita mseru ndi mkate,
Ndi moyo wace pa cakudya colongosoka.

21Mnofu wace udatha, kuti sungapenyeke;
Ndi mafupa ace akusaoneka aturuka.
22Inde wasendera kufupi ku manda,
Ndi moyo wace kwa akuononga.
23Akakhala kwa iye mthenga,
Womasulira mau mmodzi mwa cikwi,
Kuonetsera munthu comuyenera;
24Pamenepo Mulungu amcitira cifundo, nati,
Mlanditse, angatsikire kumanda,
Ndampezera dipo.
25Mnofu wace udzakhala se, woposa wa mwana;
Adzabwerera ku masiku a ubwana wace.
26Apembedza Mulungu, ndipo amkomera mtima;
M'mwemo aona nkhope yace mokondwera;
Ndipo ambwezera munthu cilungamo cace.
27Apenyerera anthu, ndi kuti,
Ndinacimwa, ndaipsa coongokaco,
Ndipo sindinapindula nako.
28Koma anandiombola ndingatsikire kumanda,
Ndi moyo wanga udzaona kuunika.
29Taona, izi zonse azicita Mulungu
Kawiri katatu ndi munthu,
30Kumbweza angalowe kumanda,
Kuti kuunika kwa moyo kumuwalire.
31Cherani khutu, Yobu, mundimvere ine;
Mukhale cete, ndipo ndidzanena ine.
32Ngati muli nao mau mundiyankhe.
Nenani, pakuti ndifuna kukulungamitsani.
33Ngati mulibe mau, tamverani Ine;
Mukhale cete, ndipo ndizakuphunzitsani nzeru.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Elihu anenetsa Mulungu sangathe kukhala wosalungama, koma asiyanitsa pakati pa okoma ndi oipa

1 Ndipo Elihu anabwereza kunena, nati,
2 Tamverani mau anga, inu anzeru;
Mundicherere khutu inu akudziwa.
3 Pakuti khutu liyesa mau,
Monga m'kamwa mulawa cakudya.
4 Tidzisankhire coyeneraco,
Tidziwe mwa tokha cokomaco.
5 Pakuti Yobu wanena, Ine ndine wolungama,
Ndipo Mulungu wandicotsera coyenera ine.
6 Kodi ndidzinamizire?
Bala langa nlosapola, ngakhale sindinalakwa.
7 Wakunga Yobu ndani,
Wakumwa mwano ngati madzi?
8 Wakutsagana nao ocita mphulupulu,
Nayendayenda nao anthu oipa.
9 Pakuti anati, Munthu sapindula kanthu nako
Kubvomerezana naye Mulu ngu.
10 Cifukwa cace mundimvere ine, eni nzeru inu,
Nkutali ndi Mulungu kucita coipa,
Ndi Wamphamvuyonse kucita cosalungama.
11 Pakuti ambwezera munthu monga mwa nchito yace,
Napezetsa munthu ali yense monga mwa mayendedwe ace.
12 Ndithu zoonadi, Mulungu sangacite coipa,
Ndi Wamphamvuyonse sangaipse mlandu.
13 Anamuikiza dziko lapansi ndani?
Kapena anakonzeratu dziko lonse lokhalamo anthu ndani?
14 Akadzikumbukila yekha mumtima mwace,
Akadzisonkhanitsira yekha mzimu wace ndi mpweya wace,
15 Zamoyo zonse zidzatsirizika pamodzi,
Ndi munthu adzabwerera kupfumbi.
16 Ngati tsono uli nako kuzindikira, tamvera ici,
Cherera khutu kunena kwanga.
17 Kodi munthu woipidwa naco ciweruzo adzalamulira?
Ndipo kodi utsutsa wolungama ndi wamphamvuyo kuti ngwoipa?
18 Kodi kuyenera kunena kwa mfumu, Wopanda pace iwe,
Kapena kwa akalonga, Oipa inu?
19 Nanga kwa Iye wosasamalira nkhope za akalonga,
Wosasiyanitsa pakati pa wolemera ndi wosauka?
Pakuti onsewo ndiwo nchito ya manja ace.
20 M'kamphindi akufa, ngakhale pakati pa usiku,
Anthu agwedezeka, napita,

Amphamvu acotsedwa opanda dzanja lakuwacotsa.
21Pakuti maso ace ali pa njira ya munthu ali yense,
Napenya moponda mwace monse.
22Palibe mdima kapena mthunzi wa imfa,
Kuti ocita zopanda pace abisaleko.
23Pakuti Mulungu alibe cifukwa ca kulingiriranso za munthu,
Kuti afike kwa Iye kudzaweruzidwa.
24Aphwanya eni mphamvu osaturutsa kubwalo mlandu wao,
Naika ena m'malo mwao.
25Pakuti asamalira nchito zao,
Nawagubuduza usiku kuti aphwanyike.
26Awakantha ngati oipa,
Poyera pamaso pa anthu.
27Popeza anapambuka, naleka kumtsata,
Osasamalira njira zace ziri zonse.
28M'mwemo anafikitsa kwa Iye kupfuula kwa osauka;
Ndipo anamva Iye kupfuula kwa ozunzika.
29Iye akapatsa mpumulo adzamtsutsa ndani?
Akabisa nkhope yace adzampenyerera ndani?
Cikacitika pa mtundu wa anthu, kapena pa munthu, ncimodzimodzi;
30Kuti munthu wonyoza Mulungu asacite ufumu,
Ndi anthu asakodwe mumsampha,
31Pakuti pali wina kodi anati kwa Mulungu,
Ndasenza kulanga kwanu, ndingakhale sindinalakwa?
32Cimene sindiciona mundilangize ndi Inu,
Ngati ndacita cosalungama sindidzabwerezanso.
33Kodi cilango ca Mulungu cikhale monga mucifuna inu, pakuti mucikana?
Musankhe ndi inu, ine ai;
M'mwemo monga mudziwa, nenani.
34Anthu ozindikira adzanena nane,
Inde anthu anzeru onse akundimva adzati,
35Yobu alankhula wopanda kudziwa,
Ndi mau ace alibe nzeru.
36Mwenzi nayesedwe Yobu kufikira kutha,
Cifukwa ca kuyankha kwace monga anthu amphulupulu,
37Pakuti pa kucimwa kwace aonjeza kupikisana ndi Mulungu,
Asansa manja pakati pa ife,
Nacurukitsa maneno ace pa Mulungu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Elihu akuti kwa Mulungu kulibe cifukwa ca kucita tsankhu

1 Ndipo Elihu anabwereza kunena, nati,
2 Kodi muciyesa coyenera,
Umo mukuti, Cilungamo canga ciposa ca Mulungu,
3 Pakuti munena, Upindulanji naco?
Posacimwa ndinapindula ciani cimene sindikadapindula pocimwa?
4 Ndidzakuyankhani,
Ndi anzanu pamodzi ndi inu.
5 Yang'anani kumwamba, nimuone,
Tapenyani mitambo yokwera yakuposa inu.
6 Ngati mwacimwa, mumcitira Iye ciani?
Zikacuruka zolakwa zanu, mumcitira Iye ciani?
7 Mukakhala wolungama, mumninkhapo ciani?
Kapena alandira ciani pa dzanja lanu?
8 Coipa canu cikhoza kuipira munthu wonga inu,
Ndi cilungamo canu cikhoza kukomera wobadwa ndi munthu.
9 Cifukwa ca kucuruka masautso anthu anapfuula,
Apfuula cifukwa ca dzanja la amphamvu.
10 Koma palibe anganene, Ali kuti Mulungu Mlengi wanga,
Wakupatsa nyimbo usiku;
11 Wakutilangiza ife koposa nyama za padziko,
Wakutipatsa nzeru zoposa mbalame za m'mlengalenga?
12 Apo apfuula, koma Iye sawayankha;
Cifukwa ca kudzikuza kwa anthu oipa.
13 Zedi Mulungu samvera zacabe,
Ndi Wamphamvuyonse sazisamalira.
14 Inde mungakhale munena, Sindimpenya,
Mlanduwo uli pamaso pace, ndipo mumlindira.
15 Ndipo tsopano popeza analibe kumzonda m'kukwiya kwace,
Ndi kusamalitsa colakwa,
16 Cifukwa cace Yobu anatsegula pakamwa pace mwacabe,
Nacurukitsa mau opanda nzeru.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Elihu alemekeza cilungamo ndi mphamvu ya Mulungu.
Mulungu ndi wangwiro, ife tilephera kumdziwa

1 Elihu nabwereza, nati,
2 Mundilole pang'ono, ndidzakuuzani,
Pakuti ndiri naonso mau akunenera Mulungu.
3 Ndidzatenga nzeru zanga kutali,
Ndidzabvomereza kuti Mlengi wanga ndi wolungama.
4 Pakuti zoonadi, mau anga sali abodza,
Wakudziwitsa mwangwiro ali nanu.
5 Taonani, Mulungu ndiye mwini mphamvu, ndipo sapeputsa munthu;
Mphamvu ya nzeru zace ndi yaikuru.
6 Sasunga woipa akhale ndi moyo,
Koma awaninkha ozunzikazowayenera iwo.
7 Sawacotsera wolungama maso ace,
Koma pamodzi ndi mafumu pa mpando wao
Awakhazika cikhazikire, ndipo akwezeka.
8 Ndipo akamangidwa m'nsinga,
Nakakodwa ndi zingwe za mazunzo,
9 Pamenepo awafotokozera nchito zao,
Ndi zolakwa zao, kuti anacita modzikuza.
10 Awatseguliranso m'khutu mwao kuti awalangize,
Nawauza abwerere kuleka mphulupulu.
11 Akamvera ndi kumtumikira,
Adzatsiriza masiku ao modala,
Ndi zaka zao mokondwera.
12 Koma akapanda kumvera adzatayika ndi lupanga,
Nadzatsirizika osadziwa kanthu.
13 Koma iwo a mtima wakunyoza Mulungu, akundika mkwiyo,
Akawamanga Iye, sapfuulira.
14 Iwowa akufa akali biriwiri,
Ndi moyo wao utayika ngati odetsedwa.
15 Apulumutsa wozunzika mwa kuzunzika kwace,
Nawatsegulira m'khutu mwao mwa kupsinjika kwao.
16 Inde akadakukopani mucoke posaukira,
Mulowe kucitando kopanda copsinja;
Ndipo zoikidwa pagome panu zikadakhala zonona ndithu.
17 Koma mukadzazidwa nazo zolingirira oipa,
Zolingirirazo ndi ciweruzo zidzakugwiranibe,
18 Pakuti mucenjere, mkwiyo ungakunyengeni mucite mnyozo;
Ndipo usakusokeretseni ukulu wa dipoli.
19 Cuma canu cidzafikira kodi, kuti simudzakhala wopsinjika,
Kapena mphamvu yanu yonse yolimba?

20Musakhumbe usiku,
Umene anthu alikhidwe m'malo mwao.
21Cenjerani, musaluniike kumphulupulu;
Pakuti mwaisankha iyi mutazunzidwa.
22Taonani, Mulungu acita mokwezeka mu mphamvu yace,
Mphunzitsi wakunga Iye ndani?
23Anamuikira njira yace ndani?
Adzati ndani, Mwacita cosalungama?
24Kumbukilani kuti mukuze nchito zace,
Zimene anaziyimbira anthu.
25Anthu onse azipenyerera,
Anthu aziyang'anira kutali.
26Taonani, Mulungu ndiye wamkuru, ndipo sitimdziwa;
Ciwerengo ca zaka zace ncosasanthulika.
27Pakuti akweza madontho a mvula,
Akhetsa mvula ya m'nkhungu yace
28Imene mitambo itsanulira,
Nibvumbitsira anthu mocuruka.
29Pali munthu kodi wodziwitsa mayalidwe a mitambo,
Ndi kugunda kwa msasa wace?
30Taonani, Iye ayala kuunika kwace pamenepo.
Nabvundikira kunsi kwace kwa nyanja.
31Pakuti aweruza nazo mitundu ya anthu.
Apatsa cakudya cocuruka.
32Akutidwa manja ace ndi mphezi,
Nailamulira igwere pofunapo Iye.
33Kugunda kwace kulalikira za Iye,
Zoweta zomwe zilota mtambo woyandikira.

©The Bible Society of Malawi, 1992

1Pa icinso mtima wanga unienjemera,
Nusunthika m'malo mwace.
2Mvetsetsani cibumo ca mau ace,
Ndi kugunda koturuka m'kamwa mwace.
3Akumveketsa pansi pa thambo ponse,
Nang'anipitsa mphezi yace ku malekezero a dziko lapansi.
4Mau abuma kuitsata,
Agunda ndi mau a ukulu wace,
Ndipo sailetsa atamveka mau ace,
5Mulungu agunda modabwitsa ndi mau ace,
Acita zazikuru osazidziwa ife.
6Pakuti anena kwa cipale cofewa, Ugwe padziko.
Momwemonso kwa mvula,
Ndi kwa mbvumbi waukuru.
7Atsekereza mokhomera cizindikilo dzanja la munthu ali yense,
Kuti anthu onse anawalenga adziwe.
8Pamenepo zirombo zilowa mobisalamo,
Nizikhala m'ngaka mwao.
9M'cipinda mwace muturuka kabvumvulu,
Ndi cisanu cifuma kumpoto.
10Mwa kupuma kwace apereka cipale,
Ndi madzi acitando aundana.
11Asenzetsanso mtambo wakuda bii madzi,
Afunyulula mtambo wokhalamo mphezi yace;
12Ndipo utembenuka-tembenuka pakulangiza kwace,
Kuti ucite ziri zonse aulamulira,
Pa nkhope ya dziko lokhalamo anthu;
13Ngati aufikitsira dziko lace kulidzudzula,
Kapena kulicitira cifundo.
14Tamverani ici, Yobu.
Taimani, mulingirire zodabwiza za Mulungu.
15Kodi mudziwa umo Mulungu azilangizira zimenezi,
Nawalitsa mphezi ya m'mtambo mwace?
16Kodi mudziwa madendekeredwe ace a mitambo,
Zodabwiza za Iye wakudziwa mwangwiro?
17Kodi mudziwa umo zobvala zanu zifundira,
Pamene dziko liri thuu cifukwa ca mwela?
18Kodi muyala thambo pamodzi ndi Iye,
Ndilo lolimba ngati kalirole woyengeka?
19Mutilangize cimene tidzanena ndi Iye;
Sitidziwa kulongosola mau athu cifukwa ca mdima.
20Kodi munthu ayenera kumuuza kuti ndifuna kunena,
Kapena kodi munthu adzakhumba kumezedwa?

21Ndipo tsopano anthu sakhoza kupenyerera kuunika
pakunyezimira kuthambo,
Ndi mphepo yapita ndi kuuyeretsa,
22Kucokera kumpoto kudzera kuwala konyezimira,
Mulungu ali nao ukulu woopsa.
23Kunena za Wamphamvuyonse, sitingamsanthule; ndiye wa
mphamvu yoposa;
Koma mwa ciweruzo ndi cilungamo cocuruka samasautsa.
24M'mwemo anthu amuopa,
Iye sasamalira ali yense wanzeru mumtima.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Mulungu aonekera kwa Yobu osamtsutsa. Koma amkumbutsa za ukuru wopambana wa Mulungu. Yobu adzicepetsapo

1 Pamenepo Yehova anayankha Yobu m'kabvumvulu, nati,
2 Ndani uyu adetsa uphungu,
Ndi mau opanda nzeru?
3 Udzimangire m'cuuno tsono ngati mwamuna;
Ndikufunsa, undidziwitse.
4 Unali kuti muja ndinaika maziko a dziko lapansi?
Fotokoza ngati udziwa kuzindikira.
5 Analemba malire ace ndani, papeza udziwa?
Anayesapo cingwe cace ndani?
6 Maziko ace anakumbidwa pa ciani?
Kapena anaika ndani mwala wace wa pangondya,
7 Muja nyenyezi za m'mawa zinayimba limodzi mokondwera,
Ndi ana onse a Mulungu anapfuula ndi cimwemwe?
8 Kapena anatseka nyanja ndani ndi zitseko,
Muja idakamula ngati kuturuka m'mimba,
9 Muja ndinayesa mtambo cobvala cace,
Ndi mdima wa bii nsaru yace yakulunga,
10 Ndi kuilembera malire anga,
Ndi kuika mipikizo ndi zitseko,
11 Ndi kuti, Ufike mpaka apa, osapitirirapo;
Apa adzaletseka mafunde ako odzikuza?
12 Kodi walamulira m'mawa ciyambire masiku ako,
Ndi kudziwitsa mbanda kuca malo ace;
13 Kuti agwire malekezero a dziko lapansi,
Nakutumule oipa acokeko?
14 Lisandulika ngati dothi lonyata pansi pa cosindikiza,
Ndi zonse zibuka ngati cobvala;
15 Ndi kuunika kwa oipa kuletsedwa kuti asakuone,
Ndi dzanja losamulidwa lityoledwa.
16 Kodi unalowa magwero a nyanja?
Kodi unayendayenda pozama peni peni?
17 Kodi zipata za imfa zinabvumbulukira iwe?
Kapena kodi unaona zipata za mthunzi wa imfa?
18 Kodi unazindikira citando ca dziko lapansi?
Fotokozera, ngati ucidziwa conse.
19 Iri kuti njira yomukira pokhala kuunika?
Ndi mdima, pokhala pace pali kuti,
20 Kuti upite nao ku malire ace,
Kuti uzindikire miseu ya ku nyumba yace?
21 Udziwa, pakuti unabadwa pamenepo,

Ndi masiku ako acuruka kuwerenga kwao.
22Kodi unalowa m'zosungiramo cipale cofewa?
Kapena unapenya zosungiramo matalala,
23Amene ndiwasungira tsiku la nsautso,
Tsiku lakulimbana nkhondo?
24Njira iri kuti yomukira pogawikana kuunika,
Kapena pomwazikira mphepo ya kum'mawa pa dziko lapansi?
25Ndani anacikumbira mcera cimvula,
Kapena njira ya bingu la mphezi,
26Kubvumbitsa mvula pa dziko lapanda anthu,
Ku cipululu kosakhala munthu,
27Kukhutitsa thengo la kunkhwangwala,
Ndi kuphukitsa msipu?
28Kodi mvula iri naye atate?
Kapena wabala ndani madontho amame?
29Cipale cinaturuka m'inimba ya yani?
Ndi cisanu cocokera m'mwamba anacibala ndani?
30Madzi aundana ngati mwala,
Ndi pamwamba pa nyanja yozama mpogwirana madzi.
31Kodi ungamange gulu la Nsangwe?
Kapena kumasula zomangira za Akamwiniatsatana?
32Ungaturutse kodi nyenyezi m'nyengo zao monga mwa malongosoledwe ao?
Kapena kutsogolera Mlalang'amba ndi ana ace?
33Kodi udziwa malemba a kuthambo?
Ukhoza kukhazikitsa ufumu wao pa dziko lapansi?
34Kodi udziwa kukwezera mau ako kumitambo,
Kuti madzi ocuruka akukute?
35Kodi ukhoza kutumiza mphezi kuti zimuke,
Ndi kunena nawe, Tiri pano?
36Ndani analonga nzeru m'mitambomo?
Ndani waninkha nyenyezi yotsotsoka luntha?
37Adziwa ndani kuwerenga mitambo mwanzeru,
Ndi kutsanulira micenje ya kuthambo ndani,
38Pokandika pfumbi,
Ndi kuundana zibuma pamodzi?
39Kodi ukhoza kusakira mkango waukazi nyama?
Ndi kukwaniritsa cakudya ca misona,
40Pamene ibwathama m'ngaka mwao,
Nikhala mobisala kulaliramo?
41Amkonzeratu khungubwi cakudya cace ndani,
Pamene ana ace apfuulira kwa Mulungu,
Nauluka-uluka osowa cakudya?

©The Bible Society of Malawi, 1992

1Kodi udziwa nyengo yakuswana zinkhoma?
Kodi wapenyerera pakuswa nswala?
2Ukhoza kodi kuwerenga miyezi yakuzipitira,
Kapena udziwa nyengo yoti ziswane?
3Zithuntha, ziswa,
Zitaya zowawa zao.
4Ana ao akhala ojinca, akulira kuthengo,
Acoka osabwerera kwa amao.
5Ndani walola mbidzi ituruke yaufulu?
Anaimasulira mbidzi nsinga zace ndani,
6Imene ndaciyesa cipululu nyumba yace,
Ndi dziko lakhulo pokhala pace?
7Aseka phokoso la kumudzi,
Osamva kukuwa kwa wofulumiza nyama za m'goli.
8Poyenda ponse pamapiri mpa busa pace;
Ilondola caciwisi ciri conse.
9Kodi njati idzabvomera kukutumikira,
Idzakhala ku codyetseramo cako kodi?
10Kodi ukhoza kumanga njati ndi lamba lace ilime m'mcera?
Kapena idzakutsata kodi kufafaniza nthumbira m'zigwa?
11Udzaikhulupirira kodi, popeza mphamvu yace njaikuru?
Udzaisiyira nchito yako kodi?
12Kodi udzaitama kuti itute mbeu zako,
Ndi kuzisonkhanitsira kudwale?
13Phiko la nthiwatiwa likondwera,
Koma mapiko ndi nthenga zace nzofatsa kodi?
14Pakuti isiya mazira ace panthaka,
Nimafunditsa m'pfumbi,
15Niiwala kuti phazi lingawaphwanye,
Kapena cirombo cingawapondereze.
16Ilumira mtima ana ace monga ngati sali ace;
Idzilemetsa ndi nchito cabe, popeza iribe mantha;
17Pakuti Mulungu anaimana nzeru,
Ndipo sanaigawira luntha.
18Ikafika nthawi yace, iweramuka,
Iseka kavalo ndi wa pamsana pace.
19Wampatsa kavalo mphamvu yace kodi?
Wambveka pakhosi pace cenjerere cogwedezeka?
20Wamlumphitsa kodi ngati dzombe?
Ulemerero wa kumina kwace ngwoopsa.
21Apalasa kucigwa, nakondwera nayo mphamvu yace;
Aturuka kukomana nao eni zida.
22Aseka mantha osaopsedwa,

Osabwerera kuthawa lupanga.
23Phodo likuti koco koco panthiti pace,
Mkondo wonyezimira ndi nthungo yomwe.
24Ndi kunjenjemera kwaukali aimeza nthaka,
Osaimitsika pomveka lipenga.
25Pomveka lipenga akuti, Hee!
Anunkhiza nkhondo irikudza kutali
Kugunda kwa akazembe ndi kuhahaza,
26Kodi kabawi auluka mwa nzeru zako,
Natambasula mapiko ace kumka kumwera?
27Kodi ciombankhanga cikwera m'mwamba pocilamulira iwe,
Nicimanga cisanja cace m'mwamba?
28Kwao nku thanthwe, cigona komweko,
Pansonga pa thanthwe pokhazikikapo.
29Pokhala kumeneko ciyang'ana cakudya;
Maso ace acipenyetsetsa ciri kutali,
30Ana ace akumwa mwazi,
Ndipo pomwe pali ophedwa, apo pali ico.

©The Bible Society of Malawi, 1992

1Ndipo Yehova anabwereza kwa Yobu, nati,
2Kodi wodzudzulayo atsutsane ndi Wamphamvuyonse?
Wocita makani ndi Mulungu ayankhe.
3Pamenepo Yobu anayankha Yehova, nati,
4Taonani, ndakhululuka ine, ndidzakubwezerani mau otani?
Ndigwira pakamwa.
5Ndalankhula kamodzi, koma sindidzayankha;
Inde kawiri, koma sindionjezanso.
6Ndipo Yehova anamyankha Yobu m'kabvumvulu, nati,
7Dzimangire m'cuuno tsono ngati mwamuna;
Ndidzakufunsa, undidziwitse.
8Cingakhale ciweruzo canga udzacityola kodi?
Udzanditsutsa kuti ndiri woipa kodi, kuti ukhale wolungama ndiwe?
9Kodi uli nalo dzanja ngati Ine Mulungu?
Kapena ukhoza kugunda ndi mau ngati Ine?
10Udzikometsere tsono ndi ukulu ndi kukuzika,
Nubvale ulemu ndi ulemerero.
11Tsanulira mkwiyo wako wosefuka,
Nupenyerere ali yense wodzikuza ndi kumcepetsa,
12Upenyerere ali yense wodzikuza, numtsitse,
Nupondereze oipa pomwe akhala.
13Uwakwirire pamodzi m'pfumbi,
Uzimange nkhope zao pobisika.
14Pamenepo inenso ndidzakubvomereza,
Kuti dzanja lako lako lamanja likupulumutsa.
15Tapenya tsono mvuu ndinaipanga pamodzi ndi iwe,
Ikudya udzu ngati ng'ombe.
16Tapenya tsono, mphamvu yace iri m'cuuno mwace,
Ndi kulimbalimba kwace kuli m'mitsempha ya m'mimba yace.
17Igwedeza mcira wace ngati mkungudza;
Mitsempha ya ncafu zace ipotana.
18Mafupa ace akunga misiwe yamkuwa;
Ziwalo zace zikunga zitsulo zamphumphu,
19Iyo ndiyo ciyambi ca macitidwe a Mulungu;
Wakuilenga anaininkha lupanga lace.
20Pakuti mapiri aiphukitsira cakudya,
Kumene zisewera nyama zonse za kuthengo,
21Igona pansi patsinde pa mitengo yamthunzi,
Pobisala pabango ndi pathawale.
22Mitengo yamthunzi iiphimba ndi mthunzi wao,
Misondodzi ya kumtsinje iizinga.
23Taona madzi a mumtsinje akakula, siinjenjemera;
Ilimbika mtima, ngakhale Yordano atupa mpaka pakamwa pace,

24Ikakhala maso, munthu adzaigwira kodi?
Kapena kuboola m'mphuno mwace iri m'khwekhwe?

©The Bible Society of Malawi, 1992

1Kodi ukhoza kukoka ng'ona ndi mbedza?
Kapena kukanikiza kalandira wace ndi cingwe?
2Kodi ukhoza kumanga m'mphuno ndi mlulu?
Kapena kuboola nsagwada wace ndi momba?
3Kodi idzacurukitsa mau akukupembedza?
Kapena idzanena nawe mau ofatsa?
4Kodi idzapangana ndi iwe,
Kuti uitenge ikhale kapolo wako wacikhalire?
5Kodi udzasewera nayo ngati mbalame?
Kapena udzaimangira anamwali ako kuti aiwete?
6Kodi opangana malonda adzaitsatsa?
Adzaigawana eni malonda?
7Kodi udzadzaza khungu lace ndi nchetho,
Kapena mutu wace ndi miomba?
8Isanjike dzanja lako;
Ukakumbukila nkhondoyi, sudzateronso.
9Taona, ciyembekezo cako ca pa iyo cipita pacabe.
Kodi sadzatenga nkhawa munthu pakungoiona?
10Palibe wolimba mtima kuti adzaiputa.
Ndipo ndaniyo adzaima pamaso pa Ine?
11Ndaniyo anayamba kundipatsa Ine kuti ndimthokoze?
Ziri zonse pansi pa thambo ponse ndi zanga.
12Sindikhala cete osachula ziwalo za ng'onayo,
Ndi mbiri ya mphamvu yace, ndi makonzedwe ace okoma.
13Ndani adzasenda cobvala cace cakunja?
Adzalowa ndani ku mizere iwiri ya mano ace?
14Adzatsegula ndani zitseko za pakamwa pace?
Mano ace aopsa pozungulira pao.
15Maamba ace olimba ndiwo kudzitama kwace;
Amangika pamodzi ngati okomeredwatu.
16Alumikizana lina ndi linzace,
Mphepo yosalowa pakati pao.
17Amamatirana lina ndi linzace,
Agwirana osagawanikana.
18Pakuyetsemula ing'anipitsa kuunika,
Ndi maso ace akunga zikope za m'mawa.
19M'kamwa mwace muturuka miuni,
Mbaliwali za moto zibukamo.
20M'mphuno mwace muturuka utsi,
Ngati nkhali yobwadamuka ndi moto wa zinyatsi.
21Mpweya wace uyatsa makara,
Ndi m'kamwa mwace muturuka lawi la moto.
22Kukhosi kwace kukhala mphamvu,

Ndi mantha abvumbuluka patsogolo pace,
23Nyama yace yopsapsala igwirana
Ikwima pathupi pace yosagwedezeka.
24Mtima wace ulimba ngati mwala,
Inde ulimba ngati mwala wa mphero,
25Ikanyamuka, amphamvu acita mantha;
Cifukwa ca kuopsedwa azimidwa nzeru.
26Munthu akaiyamba ndi lupanga, ligoma;
Ngakhale nthungo, kapena mubvi, kapena mkondo.
27Citsulo iciyesa phesi,
Ndi mkuwa ngati mtengo woola.
28Mubvi suithawitsa,
Miyala ya pacoponyera iisandutsa ciputu,
29Zibonga ziyesedwa ciputu,
Iseka kuthikuza kwace kwa nthungo,
30Kumimba kwace ikunga mapale akuthwa,
Itasalala kuthope ngati copunthira.
31Icititsa nthubwinthubwi pozama ngati nkhali,
Isanduliza nyanja ikunge mafuta.
32Icititsa mifunde yonyezimira pambuyo pace;
Munthu akadati pozama pali ndi imvi.
33Pa dziko lapansi palibe cina colingana nayo,
Colengedwa copanda mantha.
34Ipenya ciri conse codzikuza, Ndiyo mfumu ya zodzitama zonse.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Yobu adzicepetsa pamaso pa Mulungu, mabwenziwo adzudzulidwa ndi Mulungu, Yobu apulumutsidwa nadalitsidwanso

1Pamenepo Yobu anayankha Mulungu, nati,
2Ndidziwa kuti mukhoza kucita zonse,
Ndi kuti palibe coletsa colingirira canu ciri conse,
3Ndani uyu abisa uphungu wosadziwa kanthu?
Cifukwa cace ndinafotokozera zimene sindinazizindikira,
Zondidabwiza, zosazidziwa ine,
4Tamverani tu, ndidzanena ine,
Ndidzakufunsani, mundidziwitse.
5Kumva ndidamva mbiri yanu,
Koma tsopano ndikupenyani maso;
6Cifukwa cace ndekha ndidzinyansa, ndi kulapa
M'pfumbi ndi mapulusa.
7Kunali tsono atanena Yehova mau awa kwa Yobu, Yehova anati kwa Elifazi wa ku Temani, Mkwiyo wanga wakuyakira iwe ndi mabwenzi ako awiri, pakuti simunandinenera coyenera monga ananena mtumiki wanga Yobu. 8Ndipo tsono, mudzitengere ng'ombe zisanu ndi ziwiri, ndi nkhosa zamphongo zisanu ndi ziwiri, mumuke kwa mtumiki wanga Yobu, mudzifukizire nokha nsembe yopsereza; ndi mtumiki wanga Yobu adzapempherera inu, pakuti ndidzambvomereza iyeyu, kuti ndisacite nanu monga mwa kupusa kwanu; popeza simunandinenera coyenera monga ananena mtumiki Yobu. 9Namuka Elifazi wa ku Temani, ndi Bilidadi Msuki, ndi Zofara wa ku Naama, nacita monga Yehova adawauza; ndipo Yehova anabvomereza Yobu. 10Ndipo Yehova anacotsa ukapolo wa Yobu, pamene anapempherera mabwenzi ace; Yehova nacurukitsa zace zonse za Yobu mpaka kuziwirikiza. 11Pamenepo anamdzera abale ace onse, ndi alongo ace onse, ndi onse odziwana naye kale, nadya naye mkate m'nyumba yace, nampukusira mitu, namtonthoza pa zoipa zonse Yehova anamfikitsirazi; nampatsanso yense ndarama ndi mphete yagolidi. 12Ndipo Yehova anadalitsa citsiriziro ca Yobu koposa ciyambi cace, ndipo anali nazo nkhosa zikwi khumi ndi zinai, ndi ngamila zikwi zisanu ndi cimodzi, ndi ng'ombe zamagoli cikwi cimodzi, ndi aburu akazi cikwi cimodzi. 13Anali naonso ana amuna asanu ndi awiri ndi ana akazi atatu. 14Ndipo anamucha dzina la woyamba Yemima, ndi dzina la waciwiri Keziya, ndi dzina la wacitatu Kerenihapuki. 15Ndipo m'dziko monse simunapezeka akazi okongola ngati ana akazi a Yobu, nawapatsa colowa atate wao pamodzi ndi alongo ao. 16Ndipo zitatha izi, Yobu anakhala ndi moyo zaka zana limodzi mphambu

makumi anai, naona ana ace ndi zidzukulu zace mibadwo inai. 17Namwalira Yobu, wokalamba ndi wa masiku ocuruka.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Psalms

Masalmo 1

Kusiyana pakati pa olungama ndi oipa

1WODALA munthuyo wosayenda mu uphungu wa oipa,
Kapena wosaimirira m'njira ya ocimwa,
Kapena wosakhala pansi pa bwalo la onyoza.
2Komatu m'cilamulo ca Yehova muli cikondwerero cace;
Ndipo m'cilamulo cace amalingima usana ndi usiku.
3Ndiye akunga mtengo wooka pa mitsinje ya madzi;
Wakupatsa cipatso cace pa nyengo yace,
Tsamba lace lomwe losafota;
Ndipo zonse azicita apindula nazo.
4Oipa satero ai;
Koma akunga mungu wouluka ndi mphepo.
5Cifukwa cace oipa sadzaimirira pa mlanduwo,
Kapena ocimwa mu msonkhano wa olungama.
6Pakuti Yehova adziwa mayendedwe a olungama;
Koma mayendedwe a oipa adzatayika.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 2

Ufumu wa wodzozedwa wa Yehova

1Aphokoseranji amitundu.
Nalingiriranji anthu zopanda pace?
2Adzikhazikitsa mafumu a dziko lapansi,
Nacita upo akulu pamodzi,
Kutsutsana naye Yehova, ndi Wodzozedwa wace, ndi kuti.
3Tidule zomangira zao,
Titaye nsinga zao.
4Wokhala m'mwambayo adzaseka;
Ambuye adzawanyoza.
5Pomwepo adzalankhula nao mu mkwiyo wace,
Nadzawaopsa m'ukali wace:
6Koma Ine ndadzoza mfumu yanga
Pa Ziyoni, phiri langa loyera.
7Ndidzauza za citsimikizo:
Yehova ananena ndi
Ine, Iwe ndiwe Mwana wanga;
Ine lero ndakubala.
8Undifunse, ndipo ndidzakupatsa amitundu akhale colowa cako,
Ndi malekezero a dziko lapansi akhale ako ako.
9Udzawatyola ndi ndodo yacitsulo;
Udzawaphwanya monga mbiya yawoumba.
10Tsono, mafumu inu, citani mwanzeru:
Langikani, oweruza inu a dziko lapansi.
11Tumikirani Yehova ndi mantha,
Ndipo kondwerani ndi cinthenthe.
12Mpsompsoneni Mwanayo, kuti angakwiye, ndipo mungatayike m'njira,
Ukayaka pang'ono pokha mkwiyo wace.
Odala onse akumkhulupirira Iye.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 3

Kukhulupirika kwa Mulungu

Salimo la Davide, muja anathawa Abisalomu mwana wace.

1Yehova! Ha! acuruka nanga akundisautsa ine!
Akundiukira ine ndi ambiri.
2Ambiri amati kwa moyo wanga,
Alibe cipulumutso mwa Mulungu.
3Ndipo Inu Yehova, ndinu cikopa canga;
Ulemerero wanga, ndi wondiweramutsa mutu wanga.
4Ndipfuula kwa Yehova ndi mau anga,
Ndipo andiyankha m'phiri lace loyera,
5Ndinagona ine pansi, ndinagona tulo;
Ndinauka; pakuti Yehova anandicirikiza.
6Sindidzaopa unyinji wa anthu akundizinga ine.
7Ukani Yehova; ndipulumutseni, Mulungu wanga!
Pakuti mwapanda adani anga onse patsaya;
Mwawatyola mano oipawo.
8Cipulumutso nca Yehova;
Dalitso lanu likhale pa anthu anu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 4

Pemphero posautsidwa

Kwa Mkulu wa Nyimbo; pa Nesmoto. Salmo la Davide.

1Pakupfuula ine mundiyankhe, Mulungu wa cilungamo canga;
Pondicepera mwandikulitsira malo:
Ndicitireni cifundo, imvani pemphero langa.
2Amuna inu, ulemu wanga udzakhala wamanyazi kufikira liti?
Mudzakonda zacabe, ndi kufunafuna bodza kufikira liti?
3Koma dziwani kuti Yehova anadzipatulira yekha womkondayo
Adzamva Yehova m'mene ndimpfuulira Iye,
4Citani cinthenthe, ndipo musacimwe:
Nenani mumtima mwanu pakama panu, ndipo mukhale cete.
5Iphani nsembe za cilungamo,
Ndipo mumkhulupirire Yehova.
6Ambiri amati, Adzationetsa cabwino ndani?
Weramutsirani ife kuunika kwa nkhope yanu, Yehova.
7Mwapatsa cimwemwe mumtima mwanga,
Cakuposa cao m'nyengo yakucuruka dzinthu zao ndi vinyo wao.
8Ndi mtendere ndidzagona pansi, pomwepo ndidzagona tulo;
Cifukwa Inu, Yehova, mundikhalitsa ine, ndikhale bwino.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 5

Matsoka a oipa, madalitso a olungama

Kwa Mkulu wa Nyimbo; pa Nekiloto. Salimo la Davide.

1Mverani mau anga, Yehova,
Zindikirani kulingirira kwanga.
2Tamvetsani mau a kupfuula kwanga,
Mfumu yanga, ndi Mulungu wanga:
Pakuti kwa Inu ndimapemphera,
3M'mawa, Yehova, mudzamva mau anga;
M'mawa, ndidzakukonzerani pemphero langa, ndipo ndidzadikira.
4Pakuti Inu sindinu Mulungu wakukondwera naco coipa
Mphulupulu siikhala ndi Inu.
5Opusa sadzakhazikika pamaso panu:
Mudana nao onse akucita zopanda pace.
6Mudzaononga iwo akunena bodza:
Munthu wokhetsa mwazi ndi wacinyengo, Yehova anyansidwa naye.
7Koma ine, mwa kucuruka kwa cifundo canu ndidzalowa m'nyumba yanu:
Ndidzagwada kuyang'ana Kacisi wanu woyera ndi kuopa Inu.
8Yehova, munditsogolere m'cilungamo canu, cifukwa ca akundizondawo;
Mulungamitse njira yanu pamaso panga.
9Pakuti m'kamwa mwao mulibe mau okhazikika;
M'kati mwao m'mosakaza;
M'mero mwao ndi manda apululu:
Lilime lao asyasyalika nalo.
10Muwayese otsutsika Mulungu;
Agwe nao uphungu wao:
M'kucuruka kwa zolakwa zao muwapitikitse;
Pakuti anapikisana ndi Inu.
11Koma akondwere onse amene athawira kwa Inu,
Apfuule mokondwera kosaleka, popeza muwafungatira;
Nasekere mwa Inu iwo akukonda dzina lanu.
12Pakuti Inu, Yehova, mudzadalitsa wolungamayo;
Mudzamcinjiriza naco cibvomerezo ngati cikopa.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Davide apempha cifundo kwa Mulungu

Kwa Mkulu wa Nyimbo: pa Neginoto, pa Seminiti. Salmo la Davide.

1Yehova, musandidzudzule mu mkwiyo wanu,
Ndipo musandilange m'ukali wanu.
2Mundicitire cifundo, Yehova; pakuti ndalefuka ine:
Mundicize, Yehova; pakuti anthunthumira mafupa anga.
3Moyo wanganso wanthunthumira kwakukuru;
Ndipo Inu, Yehova, kufikira liti?
4Bwererani Yehova, landitsani moyo wanga;
Ndipulumutseni cifukwa ca kukoma mtima kwanu.
5Pakuti muimfa m'mosakumbukila Inu:
M'mandamo adzakuyamikani dani?
6Ndalema nako kuusa moyo kwanga;
Ndiyandamitsa kama wanga usiku wonse;
Mphasa yanga ndiolobza ndi misozi yanga.
7Lapuwala diso langa cifukwa ca cisoni;
Lakalamba cifukwa ca onse akundisautsa.
8Cokani kwa ine, nonsenu akucita zopanda pace;
Pakuti wamva Yehova mau a kulira kwanaa,
9Wamva Yehova kupemba kwanga;
Yehova adzalandira pemphero langa.
10Adzacita manyazi, nadzanthunthumira kwakukuru adani anga onse;
Adzabwerera, nadzacita manyazi modzidzimuka,

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 7

Adani amzinga, Davide adziponya kwa Mulungu

Syigayoni wa Davide woyimbira Yehova, cifukwa ca mau a Kumi Mbenjamini.

1Yehova Mulungu wanga, ndakhulupirira Inu:
Mundipulumutse kwa onse akundilonda, nimundilanditse;
2Kuti angamwetule moyo wanga ngati mkango,
Ndi kuukadzula, wopanda wina wondilanditsa.
3Yehova Mulungu wanga, ngati ndacita ici;
Ngati m'manja anga muli cosalungama;
4Ngati ndambwezera coipa iye woyanjana ndine;
(Inde, ndamlanditsa wondisautsa kopanda cifukwa);
5Mdani alondole moyo wanga, naupeze;
Naupondereze pansi moyo wanga,
Naukhalitse ulemu wanga m'pfumbi.
6Ukani Yehova mu mkwiyo wanu,
Nyamukani cifukwa ca ukali wa akundisautsa:
Ndipo mugalamukire ine; mwalamulira ciweruzo.
7Ndipo ukuzingeni msonkhano wa anthu;
Ndipo pamwamba pao mubwerere kumka kumwamba.
8Yehova aweruza anthu mlandu:
Mundiweruze, Yehova, monga mwa cilungamo canga, ndi ungwiro wanga uli mwa ine.
9Ithe mphulupulu ya anthu oipa, ndikupemphani, koma wolungamayo mumkhazikitse:
Pakuti woyesa mitima ndi imso ndiye Mulungu wolungama.
10Cikopa canga ciri ndi Mulungu, Wopulumutsa oongoka mtima.
11Mulungu ndiye Woweruza walungama,
Ndiye Mulungu wakukwiya masiku onse.
12Akapanda kutembenuka munthu, Iye adzanola lupanga lace;
Wakoka uta wace, naupiringidza.
13Ndipo anamkonzera zida za imfa;
Mibvi yace aipanga ikhale yansakali,
14Taonani, ali m'cikuta ca zopanda pace;
Anaima ndi cobvuta, nabala bodza.
15Anacita dzenje, nalikumba,
Nagwa m'mbuna yomwe anaikumba.
16Cobvuta cace cidzambwerera mwini,
Ndi ciwawa cace cidzamgwera pakati pamutu pace.
17Ndidzayamika Yehova monga mwa cilungamo cace;
Ndipo ndidzayimbira Yehova Wam'mwambamwamba.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Davide ayimbira ulemerero wa Mulungu, ndi ulemu umene Mulungu acitira mtundu wa anthu

Kwa Mkulu wa Nyimbo; pa Oititl. Salnto la Davide.

1Yehova, Ambuye wathu,
Dzina lanu liposadi nanga pa dziko lonse lapansi!
Inu amene munaika ulemerero wanu pa thambo la kumwamba.
2M'kamwa mwa makanda ndi oyamwamunakhazikitsamphamvu,
Cifukwa ca otsutsana ndi Inu,
Kuti muwaletse mdani ndi wobwezera cilango.
3Pakuona ine thambo la kumwamba lanu, nchito ya zala zanu,
Mwezi ndi nyenyezi, zimene munazikhazika,
4Munthu ndani kuti mumkumbukila?
Ndi mwana wa munthu kuti muceza naye?
5Pakuti munamcepsa pang'ono ndi Mulungu,
Munambveka iye korona wa ulemerero ndi ulemu.
6Munamcititsa ufumu pa nchito za manja anu;
Mudagonjetsa zonse pansi pa mapazi ace;
7Nkhosa ndi ng'ombe, zonsezo,
Ndi nyama za kuthengo zomwe;
8Mbalame za m'mlengalenga, ndi nsomba za m'nyanja.
Zopita m'njira za m'nyanja.
9Yehova, Ambuye wathu,
Dzina lanu liposadi nanga pa dziko lonse lapansi!

©The Bible Society of Malawi, 1992

Ayamikira cipulumutso cacikuru

Kwa Mkulu wa Nyimbo; pa Mut-laben. Salmo la Davide.

1Ndidzayamika Yehova ndi mtima wanga wonse;
Ndidzawerengera zodabwiza zanu zonse.
2Ndidzakondwerera ndi kusekera mwa Inu;
Ndidzayimbira dzina lanu, Wam'mwambamwamba Inu.
3Pobwerera m'mbuyo adani anga,
Akhumudwa naonongeka pankhope panu,
4Pakuti mwandiweruzira mlandu wanga;
Mwakhala pa mpando wacifumu, Woweruza wolungama.
5Mwadzudzula amitundu, mwaononga woipayo,
Mwafafaniza dzina lao ku nthawi Yomka muyaya.
6Adaniwo atha psiti, apululuka nthawi zonse;
Ndipo midziyo mwaipasula,
Cikumbukilo cao pamodzi catha.
7Koma Yehova akhala cikhalire:
Anakonzeratu mpando wacifumu wace kuti aweruze.
8Ndipo Iyeyu adzaweruza dziko lapansi m'cilungamo,
Nadzaweruza anthu molunjika.
9Ndipo Yehova adzakhala msanje kwa iye wokhalira mphanthi.
Msanje m'nyengo za nsautso;
10Ndipo iwo akudziwa dzina lanu adzakhulupirira Inu;
Pakuti, Inu Yehova, simunawasiya iwo akufuna Inu.
11Yimbirani zoyamika Yehova, wokhala ku Ziyoni;
Lalikirani mwa anthu nchito zace.
12Pakuti Iye wofuna camwazi awakumbukila;
Saiwala kulira kwa ozunzika.
13Ndicitireni cifundo, Yehova;
Penyani kuzunzika kwanga kumene andicitira ondidawo,
Inu wondinyamula kundicotsa ku zipata za imfa;
14Kuti ndibukitse lemekezo lanu lonse;
Pa bwalo la mwana wamkazi wa Ziyoni,
Ndidzakondwera naco cipulumutso canu.
15Amitundu anagwa m'mbuna imene anaikumba:
Lakodwa phazi lao muukonde anaucha.
16Anadziwika Yehova, anacita kuweruza:
Woipayo anakodwa ndi nchito ya manja ace.
17Oipawo adzabwerera kumanda,
Inde amitundu onse akuiwala Mulungu.
18Pakuti sadzaiwalika nthawi zonse waumphawi,
Kapena ciyembekezo ca ozunzika sicidzaonongeka kosatha.
19Ukani, Yehova, asalimbike munthu;
Amitundu aweruzidwe pankhope panu.

20Muwacititse mantha, Yehova; Adziwe amitundu kuti ali anthu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 10

Athamangira Mulungu pothawa adani omtsata

1Muimiranji patari, Yehova?
Mubisaliranji m'nyengo za nsautso?
2Podzikuza woipa apsereza waumphawi;
Agwe m'ciwembu anapanganaco.
3Pakuti woipa adzitamira cifuniro ca moyo wace,
Adalitsa wosirira, koma anyoza Yehova.
4Woipa, monga mwa kudzikuza kwa nkhope yace, akuti,
Sadzafunsira.
Malingaliro ace onse akuti, Palibe Mulungu.
5Mayendedwe ace alimbika nthawi zonse;
Maweruzo anu ali pamwamba posaona iye;
Adani ace onse awanyodola.
6Ati mumtima mwace, Sindidzagwedezeka ine;
Ku mibadwo mibadwo osagwa m'tsoka ine.
7M'kamwa mwace mwadzala kutemberera ndi manyengo ndi kucenjerera;
Pansi pa lilime lace pali cibvutitso copanda pace.
8Akhala m'molalira midzi;
Mobisalamo akupha munthu wosacimwa:
Ambisira waumphawi nkhope yace,
9Alalira monga mkango m'ngaka mwace;
Alalira kugwira wozunzika:
Agwira wozunzika, pakumkola m'ukonde mwace.
10Aunthama, nawerama,
Ndipo aumphawi agwa m'zala zace.
11Anena m'mtima mwace, Mulungu waiwala;
Wabisa nkhope yace; sapenya nthawi zonse,
12Ukani, Yehova; samulani dzanja lanu, Mulungu;
Musaiwale ozunzika.
13Woipa anyozeranii Mulungu,
Anena m'mtima mwace, Simudzafunsira?
14Mwapenya; pakuti mumayang'anira cibvutitso ndi cisoni kuti acipereke m'manja mwanu;
Waumphawi adzipereka kwa Inu;
Wamasiye mumakhala mthandizi wace.
15Thyolani mkono wa woipa;
Ndipo wocimwa, mutsate coipa cace kufikira simucipezanso cina.
16Yehova ndiye Mfumu ku nthawi yamuyaya;
Aonongeka amitundu m'dziko lace.
17Yehova, mwamva cikhumbo ca ozunzika:
Mudzakhazikitsa mtima wao, mudzachereza khutu lanu:
18Kuti muweruze mlandu wa amasiye ndi wokhalira mphanthi,

Kuti munthu wa pa dziko lapansi angaonjeze kuopsa.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 11

Yehova asunga anthu ace nalanga oipa

Kwa Mkulu wa Nyimbo: Salmo la Davide.

1Ndakhulupirira Yehova:
Mutani nkunena kwa moyo wanga,
Thawirani ku phiri lanu ngati mbalame?
2Pakuti, onani, oipa akoka uta,
Apiringidza mubvi wao pansinga,
Kuwaponyera mumdima oongoka mtima.
3Akapasuka maziko,
Wolungama angacitenji?
4Yehova ali m'Kacisi wace woyera,
Yehova, mpando wacifumu wace uli m'Mwamba;
Apenyerera ndi maso ace, ayesa ana a anthu ndi zikope zace.
5Yehova ayesa wolungama mtima:
Koma moyo wace umuda woipa ndi iye wakukonda ciwawa.
6Adzagwetsa pwata pwata misampha pa oipa;
Moto ndi miyala yasuifure, ndi mphepo yoopsa zidzawagawikira m'cikho cao.
7Pakuti Yehova ndiye wolungama; akonda zolungama:
Woongoka mtima adzapenya nkhope yace.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 12

Anthu ndi amabodza, Mulungu ndiye woona

Kwa Mkulu wa Nyimbo: pa Seminiti

1Pulumutsani, Yehova; pakuti wofatsa wasowa;
Pakuti okhulupirika acepa mwa ana a anthu.
2Amanena za bodza munthu yense ndi mnansi wace:
Amanena ndi mlomo wotyasika, ndi mitima iwiri.
3Yehova adzadula milomo yonse yotyasika,
Lilime lakudzitamandira:
4Amene amati, Ndi lilime lathu tidzaposa;
Milomo yathu nja ife eni; mbuye wa pa ife ndani?
5Cifukwa ca kupasuka kwa ozunzika, cifukwa ca kuusa moyo kwa aumphawi,
Ndiuka tsopano, ati Yehova; Ndidzamlonga mosungika muja alaka-lakamo.
6Mau a Yehova ndi mau oona;
Ngati siliva woyenga m'ng'anjo yadothi,
Yoiyeretsa kasanu ndi kawiri.
7Mudzawasunga, Yehova,
Mudzawacinjirizira mbadwo uno ku nthawi zonse.
8Oipa amayenda mozungulira-zungulira,
Potamanda iwo conyansa mwa ana a anthu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 13

Munkhawa athawira Mulungu namkhulupirira

Kwa Mkulu wa Nyimbo. Salmo la Davide.

1Mudzandiiwala ciiwalire, Yehova, kufikira liti?
Mudzandibisira ine nkhope yanu kufikira liti?
2Ndidzacita uphungu m'moyo mwanga kufikira liti,
Pokhala ndi cisoni m'mtima mwanga tsiku lonse?
Adzandiukira ine mdani wanga kufikira liti?
3Penyani, ndiyankheni, Yehova Mulungu wanga:
Penyetsani maso anga, kuti ndingagone tulo ta imfa;
4Kuti anganene mdani wanga, Ndamlaka;
Ndipo angakondwere otsutsana nane posunthika ine.
5Koma ine ndakhulupira pa cifundo canu;
Mtima wanga udzakondwera naco cipulumutso canu:
6Ndidzayimbira Yehova,
Pakuti anandicitira zokoma.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Anthu oipadi

Kwa Mkulu wa Nyimbo: Salmo la Davide.

1Waucitsiru amati mumtima mwace, Kulibe Mulungu.
Acita zobvunda, acita nchito zonyansa;
Kulibe wakucita bwino.
2Yehova m'Mwamba anaweramira pa ana a anthu,
Kuti aone ngati aliko wanzeru,
Wakufuna Mulungu.
3Anapatuka onse; pamodzi anabvunda mtima;
Palibe wakucita bwino ndi mmodzi yense.
4Kodi onse ocita zopanda pace sadziwa kanthu?
Pakudya anthu anga monga akudya mkate,
Ndipo saitana pa Yehova. 5Pamenepa anaopa-opatu:
Pakuti Mulungu ali mu mbadwo wa wolungama.
6Munyazitsa uphungu wa wozunzika,
Koma Yehova ndiye pothawira pace.
7Mwenzi cipulumutso ca Israyeli citacokera ku Ziyoni!
Pakubweretsa Yehova anthu ace a m'nsinga,
Pamenepo adzakondwera Yakobo, nadzasekera Israyeli.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 15

Cikhalidwe ca munthu woona wa Mulungu

Salmo la Davide.

1Yehova, ndani adzagonera m'cihema mwanu?
Adzagonera ndani m'phiri lanu lopatulika?
2Iye wakuyendayo mokwanira, nacita cilungamo,
Nanena zoonadi mumtima mwace.
3Amene sasinjirira ndi lilime lace,
Sacitira mnzace coipa,
Ndipo satola msece pa mnansi wace.
4M'maso mwace munthu woonongeka anyozeka;
Koma awacitira ulemu akuopa Yehova.
Atalumbira kwa tsoka lace, sasintha ai.
5Ndarama zace sakongoletsa mofuna phindu lalikuru,
Ndipo salandira cokometsera mlandu kutsutsa wosacimwa.
Munthu wakucita izi sadzagwedezeka ku nthawi zonse,

©The Bible Society of Malawi, 1992

Munthu wokhulupira Mulungu akhazikika mtima, osaopa kutayika

Mlkitamu wa Davide.

1Ndisungeni ine, Mulungu: pakuti ndakhulupirira Inu.
2Ndinati kwa Yehova, Inu ndinu Ambuye wanga:
Ndiribe cabwino cina coposa Inu.
3Za oyera mtima okhala pa dziko lapansi,
Iwo ndiwo omveka mbiri, mwa iwowo muli cikondwero canga conse.
4Zidzacuruka zisoni zao za iwo otsata mulungu wina:
Sindidzathira nsembe zao zamwazi,
Ndipo sindidzachula maina ao pakamwa panga,
5Yehova ndiye gawo la colowa canga ndi cikho canga:
Ndinu wondigwirira colandira canga,
6Zingwe zandigwera mondikondweretsa;
Inde cosiyira cokoma ndiri naco.
7Ndidzadalitsa Yehova, amene anandicitira uphungu:
Usikunso imso zanga zindilangiza.
8Ndaika Yehova patsogolo panga nthawi zonse:
Popeza ali pa dzanja langa lamanja, sindidzagwedezeka.
9Cifukwa cace wasekera mtima wanga, nukondwera ulemu wanga;
Mnofu wanganso udzakhala mokhazikika.
10Pakuti simudzasiya moyo wanga kumanda;
Simudzalola wokondedwa wanu abvunde.
11Mudzandidziwitsa njira ya moyo:
Pankhope panu pali cimwemwe cokwanira;
M'dzanja lanu lamanja muli zokondweretsa zomka muyaya.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Davide apempha Mulungu amsunge pa ofuna kumuononga

Pemphero la Davide.

1Yehova, imvani cilungamo, mverani mpfuu wanga;
Cherani khutu ku pemphero langa losaturuka m'milomo ya cinyengo,
2Pankhope panu paturuke ciweruzo canga;
Maso anu apenyerere zolunjika,
3Mwayesera mtima wanga; mwandizonda usiku;
Mwandisuntha, simupeza kanthu;
Ndatsimikiza mtima kuti m'kamwa mwanga simudzalakwa.
4Za macitidwe a anthu, ndaceniera ndi mau a milomo yanu
Ndingalowe njira za woononga.
5M'mayendedwe anga ndasunga mabande anu,
Mapazi anga sanaterereka.
6Ine ndinakuitanani, pakuti mudzandiyankha, Mulungu:
Cherani khutu lanu kwa ine, imvani mau anga.
7Onetsani cifundo canu codabwiza, Inu wakupulumutsa okhulupirira Inu
Kwa iwo akuwaukira ndi dzanja lanu lamanja.
8Ndisungeni monga kamwana ka m'diso,
Ndifungatireni mu mthunzi wa mapiko anu,
9Kundilanditsa kwa oipa amene andipasula,
Adani a pa moyo wanga amene andizinga.
10Mafuta ao awatsekereza;
M'kamwa mwao alankhula modzikuza.
11Tsopano anatizinga m'mayendedwe athu:
Apenyetsetsa m'maso kuti atigwetse pansi.
12Afanana ndi mkango wofuna kumwetula,
Ndi msona wa mkango wakukhala mobisalamo.
13Ukani Yehova,
Mumtsekereze, mumgwetse:
Landitsani moyo wanga kwa woipa ndi lupanga lanu;
14Kwa anthu, ndi dzanja lanu, Yehova,
Kwa anthu a dziko lapansi pano amene colowa cao ciri m'moyo uno,
Ndipo mimba yao muidzaza ndi cuma canu cobisika:
Akhuta mtima ndi ana,
Nasiyira ana amakanda zocuruka zao.
15Koma ine ndidzapenyerera nkhope yanu m'cilungamo:
Ndidzakhuta mtima ndi maonekedwe anu, pamene ndidzauka.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Nyimbo yoyamikira Yehova

Kwa Mkulu wa Nyimbo. Salmo la mtumiki wa Yehova, Davide, amene ananena kwa Yehova mau a nyimbo iyi m'mene Yehova anamlanditsa m'dzanja la adani ace onse, ndi m'dzanja la Sauli: ndipo anati,

1Ndikukondani, Yehova, mphamvu yanga.
2Yehova ndiye thanthwe langa, ndi linga langa, ndi mpulumutsi wanga;
Mulungu wanga, ngaka yanga, ndidzakhulupirira Iye;
Cikopa canga, nyanga ya cipulumutso canga, msanje wanga.
3Ndidzaitanira Yehova, woyenera kutamandika:
Ndipo adzandipulumutsa ine kwa adani anga.
4Zingwe za imfa zinandizinga,
Ndipo mitsinje ya zopanda pace inandiopsa.
5Zingwe za manda zinandizinga:
Misampha ya imfa inandifikira ine.
6M'kusauka kwanga ndinaitana Yehova,
Ndipo ndinakuwira Mulungu wanga;
Mau anga anawamva m'Kacisi mwace,
Ndipo mkuwo wanga wa pankhope pace unalowa m'makutu mwace.
7Pamenepo linagwedezeka, ndi kutenthemera dziko lapansi.
Ndi maziko a mapiri ananjenjemera
Nagwedezeka, pakuti anakwiya iyeyo.
8Unakwera utsi woturuka m'mphuno mwace:
Ndi moto wa m'kamwa mwace unanyeka:
Nuyakitsa makara.
9Ndipo Iye anaweramitsa thambo, natsika;
Ndipo pansi pa mapazi ace panali mdima bii.
10Ndipo anaberekeka pa kerubi, nauluka;
Nauluka msanga pa mapiko a mphepo,
11Anaika mdima pobisala pace, hema wace womzinga;
Mdima wa madzi, makongwa a kuthambo.
12Mwa kucezemira kunali pamaso pace makongwa anakanganuka,
Matalala ndi makala amoto.
13Ndipo anagunda m'mwamba Yehova,
Ndipo Wam'mwambamwamba anamvetsa liu lace;
Matalala ndi makala amoto,
14Ndipo anatuma mibvi yace nawabalalitsa;
Inde mphezi zaunyinji, nawamwaza.
15Ndipo zidaoneka zoyendamo madzi,
Nafukuka maziko a dziko lapansi,
Mwa kudzudzula kwanu, Yehova,
Mwa mpumo wa mpweya wa m'mphuno mwanu.

16Anatuma kucokera m'mwamba, ananditenga;
Anandibvuula m'madzi ambiri.
17Anandipulumutsa ine kwa mdani wanga wamphamvu,
Ndi kwa iwo ondida ine, pakuti anandiposa mphamvu.
18Anandipeza ine tsiku la tsoka langa;
Koma Yehova anali mcirikizo wanga.
19Ananditurutsanso andifikitse motakasuka;
Anandilanditsa, pakuti anakondwera ndi ine.
20Yehova anandibwezera monga mwa cilungamo canga;
Anandisudzula monga mwa kusisira kwa manja anga.
21Pakuti ndasunga njira za Yehova,
Ndipo sindinacitira coipa kusiyana ndi Mulungu wanga.
22Pakuti maweruzo ace onse anali pamaso panga,
Ndipo malemba ace sindinawacotsa kwa ine.
23Ndipo ndinakhala wangwiro ndi iye,
Ndipo ndinadzisunga wosacita coipa canga.
24Ndimo anandisudzulira Yehova monga mwa cilungamo canga,
Monga mwa kusisira kwa manja anga pamaso pace.
25Pa wacifundo mukhala wacifundo
Pa mumthu wangwiro mukhala wangwiro;
26Pa woyera mtima mukhala woyera mtima;
Pa wotsutsatsutsa mukhala wotsutsana naye.
27Pakuti Inu muwapulumutsa anthu aumphawi;
Koma maso okweza muwatsitsa.
28Pakuti Inu muyatsa nyali yanga;
Yehova, Mulungu wanga, aunikira mdima wanga.
29Pakuti mwa Inu ndipyola khamu la anthu;
Ndipo mwa Mulungu wanga ndilumphira linga.
30Mulungu ndiyewangwiro m'njira zace;
Mau a Yehova ngoyengeka; Ndiye cikopa ca onse okhulupirira Iye.
31Pakuti Mulungu ndani wosati Yehova?
Ndipo thanthwe ndani wosati Mulungu wathu?
32Mulungu ndiye wondizingiza mphamvu m'cuuno,
Nakonza njira yanga ikhale yangwiro.
33Alinganiza mapazi anga ngati a nswala:
Nandiimitsa pamsanje panga.
34Aphunzitsa manja anga agwire nkhondo;
Kuti walifuka uta wamkuwa ndi manja anga.
35Ndipo mwandipatsa cikopa ca cipulumutso canu:
Ndipo dzanja lamanja lanu landigwiriziza,
Ndipo cifatso canu candikuza ine.
36Mwandipondetsa patali patali,
Sanaterereka mapazi anga.
37Ndidzalondola adani anga, ndi kuwapeza:

Ndipo sindidzabwerera asanathe psiti.
38Ndidzawapyoza kuti sangakhoze kuuka:
Adzagwa pansi pa mapazi anga,
39Pakuti mwaudizingiza mphamvu m'cuuno ku nkhondoyo:
Mwandigonjetsera amene andiukira.
40Ndipo adani anga mwawalozetsa m'mbuyo kwa ine,
Kuti ndipasule ondidawo.
41Anapfuula, koma panalibewopulumutsa;
Ngakhale kwa Yehova, koma sanawabvomereza.
42Pamenepo ndinawapera ngati pfumbi la kumphepo;
Ndinawakhuthula ngati matope a pabwalo.
43Mwandipulumutsa pa zolimbana nane za anthu;
Mwandiika mutu wa amitundu;
Mtundu wa anthu sindinaudziwa udzanditumikira.
44Pakumva m'khutu za ine adzandimvera:
Alendo adzandigonjera monyenga.
45Alendo adzafota,
Nadzaturuka monjenjemera m'ngaka mwao.
46Yehova ngwa moyo; ndipo lidalitsike thanthwe langa;
Nakwezeke Mulungu wa cipulumutso canga:
47Ndiye Mulungu amene andibwe, zerera cilango,
Nandigonjetsera mitundu ya anthu.
48Andipulumutsa kwa adani anga:
Inde mundikweza pa iwo akundiukira ine:
Mundikwatula kwa munthu waciwawa.
49Cifukwa cace Yehova ndidzakuyamikani mwa amitundu,
Ndipo dzina lanu ndidzaliyimbira.
50Alanditsa mfumu yace ndi cipulumutso cacikuru:
Nacitira cifundo wodzozedwa wace,
Davide, ndi mbumba yace, ku nthawi zonse.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 19

Davide alemekeza zolengedwa ndi Mulungu, ndi malamulo ao omwe

Kwa Mkulu wa Nyimbo. Salmo la Davide

1Zakumwamba zimalalikira ulemerero wa Mulungu;
Ndipo thambo lionetsa nchito ya manja ace.
2Usana ndi usana ucurukitsa mau,
Ndipo usiku ndi usiku uonetsa nzeru.
3Palibe cilankhulidwe, palibe mau;
Liu lao silimveka.
4Muyeso wao wapitirira pa dziko lonse lapansi,
Ndipo mau ao ku malekezero a m'dziko muli anthu.
Iye anaika hema la dzuwa m'menemo,
5Ndipo liri ngati mkwati wakuturuka m'cipinda mwace,
Likondwera ngati ciphona kuthamanga m'njira.
6Kuturuka kwace lituruka kolekezera thambo,
Ndipo kuzungulira kwace lifikira ku malekezero ace:
Ndipo kulibe kanthu kobisalira kutentha kwace.
7Malamulo a Yehova ali angwiro, akubwezera moyo;
Mboni za Yehova ziri zokhazikika, zakuwapatsa opusa nzeru;
8Malangizo a Yehova ali olungama, akukondweretsa mtima:
Malamulo a Yehova ali oyera, akupenyetsa maso.
9Kuopa Yehova kuli mbe, kwakukhalabe nthawi zonse:
Maweruzo a Yehova ali oona, alungama konse konse.
10Ndizo zifunika koposa golidi, inde, golidi wambiri woyengetsa:
Zizuna koposa uci ndi zakukha za zisa zace,
11Ndiponso kapolo wanu acenjezedwa nazo:
M'kuzisunga izo muli mphotho yaikuru.
12Adziwitsa zolowereza zace ndani?
Mundimasule kwa zolakwa zobisika.
13Ndiponso muletse kapolo wanu pa zodzitama;
Zisacite ufumu pa ine: pamenepo ndidzakhala wangwiro,
Ndi wosacimwa colakwa cacikuru.
14Mau a m'kamwa mwanga ndi maganizo a m'mtima wanga
abvomerezeke pamaso panu,
Yehova, thanthwe langa, ndi Mombolo wanga,

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 20

Kupempherera mfumu poturukira iye kunkhondo

Kwa Mkulu wa Nyimbo. Salmo la Davide.

1Yehova akubvomereze tsiku la nsautso;
Dzina la Mulungu wa Yakobo likuike pamsanje;
2Likutumizire thandizo loturuka m'malo oyera,
Ndipo likugwirizize kucokera m'Ziyoni;
3Likumbukile zopereka zako zonse,
Lilandire nsembe yako yopsereza;
4Likupatse ca mtima wako,
Ndipo likwaniritse upo wako wonse.
5Tidzapfuula mokondwera mwa cipulumutso canu,
Ndipo m'dzina la Mulungu wathu tidzakweza mbendera:
Yehova akwaniritse mapempho ako onse.
6Tsopano ndidziwa kuti Yehova apulumutsa wodzozedwa wace;
Adzambvomereza m'Mwamba mwace moyera
Ndi mphamvu ya cipulumutso ca dzanja lace lamanja.
7Ena atama magareca, ndi ena akavalo:
Koma ife tidzachula dzina la Yehova Mulungu wathu.
8Iwowa anagonieka, nagwa:
Koma ife tauka, ndipo takhala ciriri.
9Yehova, pulumutsani,
Mfumuyo atibvomereze tsiku lakuitana ife.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 21

Davide ayamika Mulungu pa kugonjetsa adani

Kwa Mkulu wa Nyimbo. Salimo la Davide,

1Yehova, adzasekera mfumu mu mphamvu yanu;
Adzakondwera kwakukuru m'cipulumutso canu!
2Mwampatsa iye cikhumbo ca mtimawace,
Ndipo simunakana pempho la milomo yace.
3Pakuti mumkumika iye ndi madalitso okoma:
Muika korona wa golidi woyengetsa pamutu pace.
4Anakupemphani moyo, mwampatsa iye;
Mwamtalikitsira masiku ku nthawi za nthawi.
5Ulemerero wace ngwaukuru mwa cipulumutso canu:
Mumcitira iye ulemu ndi ukulu.
6Pakuti mumuikira madalitso ku nthawi zonse;
Mumkondweretsa ndi cimwemwe pankhope panu.
7Pakuti mfumu akhulupirira Yehova,
Ndipo mwa cifundo ca Wam'mwambamwamba sadzagwedezeka iye,
8Dzanja lanu lidzapeza adani anu onse:
Dzanja lanu lamanja lidzapeza iwo akuda Inu.
9Mudzawaika ngati ng'anjo yamoto pa nyengo ya mkwiyo wanu.
Yehova adzawatha m'kukwiya kwace,
Ndipo moto udzawanyeketsa.
10Mudzaziononga zobala zao kuzicotsa pa dziko lapansi,
Ndi mbeu zao mwa ana a anthu.
11Pakuti anakupangirani coipa:
Anapangana ciwembu, osakhoza kucicita.
12Pakuti mudzawabweza m'mbuyo,
Popiringidza m'nsinga zanu pankhope pao,
13Kwezekani, Yehova, mu mphamvu yanu:
Potero tidzayimba ndi kulemekeza cilimbiko canu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Posautsidwa Davide adandaulira, apemphera, ayamika Mulungu

Kwa Mkulu wa Nyimbo; pa Ajelet Hasakara, Salmo la Davide.

1Mulungu wanga, Mulungu wanga, mwandisiyiranji ine?
Mukhaliranji kutali kwa cipulumutso canga, ndi kwa mau a kubuula kwanga?
2Mulungu wanga, ndiitana usana, koma simubvomereza;
Ndipo usiku, sindikhala cete.
3Koma Inu ndinu woyera,
Wakukhala m'malemekezo a Israyeli.
4Makolo athu anakhulupirira Inu:
Anakhulupirira, ndipo munawalanditsa.
5Anapfuula kwa Inu, napulumutsidwa:
Anakhulupita Inu, ndipo sanacita manyazi.
6Koma ine ndine nyongolotsi, si munthu ai:
Cotonza ca anthu, ndi wonyozedwa ndi anthu.
7Onse akundipenya andiseka:
Akwenzula, apukusa mutu, nati,
8Adadzitengera kwa Yehova; kuti adzampulumutsa,
Amlanditse tsopano popeza akondwera naye.
9Pakuti Inu ndinu wondibadwitsa:
Wondikhulupiritsa pokhala ine pa bere la mai wanga.
10Cibadwire ine anandisiyira Inu:
Kuyambira kwa mai wanga Mulungu wanga ndinu.
11Musandikhalire kutali; pakuti nsautso iri pafupi:
Pakuti palibe mthandizi.
12Ng'ombe zamphongo zambiri zandizinga:
Mphongo zolimba za ku Basana zandizungulira,
13Andiyasamira m'kamwa mwao,
Ngati mkango wozomola ndi wobangula.
14Ndathiridwa pansi monga madzi,
Ndipo mafupa anga onse anaguluka:
Mtima wanga ukunga sera; Wasungunuka m'kati mwa matumbo anga,
15Mphamvu yanga yauma ngati phale;
Ndi lilime langa likangamira ku nsaya zanga;
Ndipo mwandifikitsa ku pfumbi la imfa.
16Pakuti andizinga agaru:
Msonkhano wa oipa wanditsekereza;
Andiboola m'manja anga ndi m'mapazi anga.
17Ndikhoza kuwerenga mafupa anga onse;
Iwo ayang'ana nandipenyetsetsa ine:
18Agawana zobvala zanga,

Nalota maere pa malaya anga,
19Koma Inu, Yehova, musakhale kutari;
Mphamvu yanga Inu, mufulumire kundithandiza.
20Landitsani moyo wanga kulupanga;
Wokondedwa wanga ku mphamvu ya garu,
21Ndipulumutseni m'kamwa mwa mkango;
Inde mwandiyankha ine ndiri pa nyanga za njati,
22Ndidzalalikira dzina lanu kwa abale anga:
Pakati pa msonkhano ndidzakulemekezani.
23Inu akuopa Yehova, mumlemekeze;
Inu nonse mbumba ya Yakobo, mumcitire ulemu;
Ndipo mucite mantha ndi Iye, inu nonse mbumba ya Israyeli.
24Pakuti sanapeputsa ndipo sananyansidwa ndi zunzo la wozunzika;
Ndipo sanambisira nkhope yace;
Koma pompfuulira Iye, anamva.
25Lemekezo langa lidzakhala la Inu mu msonkhano waukuru:
Zowinda zanga ndidzazicita pamaso pa iwo akumuopa Iye.
26Ozunzika adzadya nadzakhuta:
Adzayamika Yehova iwo amene amfuna:
Ukhale moyo mtima wako nthawi zonse.
27Malekezero onse a dziko lapansi adzakumbukila
nadzatembenukira kwa Yehova:
Ndipo mafuko onse a amitundu adzagwadira pamaso panu.
28Pakuti ufumuwo ngwa Yehova;
Iye acita ufumu mwa amitundu.
29Onenepa onse a pa dziko lapansi adzadya nadzagwadira:
Onse akutsikira kupfumbi adzawerama pamaso pace,
Ndi iye amene sadziwa kusunga moyo wace.
30Mbumba ya anthu idzamtumikira;
Kudzanenedwa za Ambuye ku mibadwo yakudza.
31Iwo adzadza nadzafotokozera cilungamo cace
Kwa anthu akadzabadwa, kuti Iye anacicita.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 23

Amwai amene Yehova akhala Mbusa wao

Salimo la Davide,

1Yehova ndiye mbusa wanga; sindidzasowa.
2Andigonetsa ku busa lamsipu:
Anditsogolera ku madzi ndikha.
3Atsitsimutsa moyo wanga;
Anditsogolera m'mabande a cilungamo, cifukwa ca dzina lace.
4Inde, ndingakhale ndiyenda m'cigwa ca mthunzi wa Imfa,
Sindidzaopa coipa; pakuti Inu muli ndi ine:
Cibonga canu ndi ndodo yanu, izi zindisangalatsa ine,
5Mundiyalikira gome pamaso panga m'kuona kwa adani anga:
Mwandidzoza mutu wanga mafuta; cikho canga cisefuka.
6Inde ukoma ndi cifundo zidzanditsata masiku onse a moyo wanga:
Ndipo ndidzakhala m'nyumba ya Yehova masiku onse.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 24

Ulemerero wa Yehova

Salmo la Davide,

1Dziko lapansi nla Yehova ndi zodzala zace zomwe,
Dziko lokhalamo anthu ndi iwo okhala m'mwemo.
2Pakuti Iye analimanga pazinyanja,
Nalikhazika pamadzi.
3Adzakwera ndani m'phiri la Yehova?
Nadzaima m'malo ace oyera ndani?
4Woyera m'manja, ndi woona m'mtima, ndiye;
Iye amene sanakweza moyo wace kutsata zacabe,
Ndipo salumbira monyenga,
5Iye adzalandira dalitso kwa Yehova,
Ndi cilungamo kwa Mulungu wa cipulumutso cace.
6Uwu ndi mbadwo wa iwo akufuna Iye,
Iwo akufuna nkhope yanu, Mulungu wa Yakobo.
7Weramutsani mitu yanu, zipata inu;
Ndipo kwezekani inu, zitseko zosatha:
Kuti Mfumu ya ulemerero ilowe.
8Mfumu imene ya ulemerero ndani?
Yehova wamphamvu ndi wolimba,
Yehova wolimba kunkhondo.
9Weramutsani mitu yanu, zipata inu;
Inde weramutsani, zitseko zosatha inu,
Kuti Mfumu ya ulemerero ilowe.
10Mfumu imene ya ulemerero ndani?
Yehova wa makamu makamu, Ndiye Mfumu ya ulemerero.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 25

Davide apempha Mulungu amlanditse kwa adani

Salmo la Davide.

1Ndikweza moyo wanga kwa Inu, Yehova.
2Mulungu wanga, ndakhulupirira Inu,
Ndisacite manyazi;
Adani anga asandiseke ine.
3Inde, onse akuyembekezera Inu sadzacita manyazi
Adzacita manyazi iwo amene acita monyenga kopanda cifukwa.
4Mundidziwitse njira zanu, Yehova;
Mundiphunzitse mayendedwe anu.
5Munditsogolere m'coonadi canu, ndipo mundiphunzitse;
Pakuti Inu ndinu Mulungu wa cipulumutso canga;
Inu ndikuyembekezerani tsiku lonseli.
6Kumbukilani, Yehova, nsoni zanu ndi cifundo canu;
Pakuti izi nza kale lonse,
7Musakumbukile zolakwa za ubwana wanga kapena zopikisana nanu:
Mundikumbukile monga mwa cifundo canu,
Cifukwa ca ubwino wanu, Yehova.
8Yehova ndiye wabwino ndi wolunjika mtima:
Cifukwa cace adzaphunzitsa olawa za njira.
9Adzawatsogolera ofatsa m'ciweruzo:
Ndipo adzaphunzitsa ofatsa njira yace.
10Mayendedwe onse a Yehova ndiwo cifundo ndi coonadi,
Kwa iwo akusunga pangano lace ndi mboni zace.
11Cifukwa ca dzina lanu, Yehova,
Ndikhululukireni kusakaza kwanga, pakuti ndiko kwakukuru.
12Munthuyo wakuopa Yehova ndani?
Adzamlangiza iye njira adzasankheyo.
13Moyo wace udzakhala mokoma;
Ndi mbumba zace zidzalandira dziko lapansi.
14Cinsinsi ca Yehova ciri kwa iwo akumuopa Iye;
Ndipo adzawadziwitsa pangano lace.
15Maso anga alinga kwa Yehova kosaleka;
Pakuti Iye adzaonjola mapazi anga m'ukonde.
16Ceukirani ine ndipo ndicitireni cifundo;
Pakuti ndiri woungumma ndi wozunzika.
17Masautso a mtima wanga akula:
Munditurutse m'zondipsinja.
18Penyani mazunzo anga ndi zabvuta zanga;
Ndipo khululukirani zolakwa zanga zonse.
19Penyani adani anga, popeza acuruka;
Ndipo andida ndi udani waciwawa.

20Sungani moyo wanga, ndilanditseni,
Ndisakhale nao manyazi, pakuti ndakhulupirira Inu.
21Ungwiro ndi kuongoka mtima zindisunge,
Pakuti ndayembekezera Inu.
22Ombolani Israyeli, Mulungu, M'masautso ace onse.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Davide popempha Mulungu amweruze, achula zokoma zace

Salmo la Davide.

1Mundiweruze, Yehova, pakuti ndayenda m'ungwiro wanga:
Ndipo ndakhulupirira Yehova, sindidzaterereka.
2Mundiyesere, Yehova, ndipo mundisunthe;
Yeretsani imso zanga ndi mtima wanga.
3Pakuti cifundo canu ciri pamaso panga;
Ndipo ndayenda m'coona canu.
4Sindinakhala pansi ndi anthu acabe;
Kapena kutsagana nao anthu otyasika.
5Ndidana nao msonkhano wa ocimwa,
Ndipo sindidzakhala nao pansi ocita zoipa.
6Ndidzasamba manja anga mosalakwa;
Kuti ndizungulire guwa la nsembe lanu, Yehova:
7Kuti ndimveketse mau a ciyamiko,
Ndi kulalikira nchito zanu zonse zozizwa.
8Yehova, ndikonda cikhalidwe ca nyumba yanu,
Ndi malo akukhalamo ulemerero wanu.
9Musandicotsere mzimu wanga pamodzi ndi olakwa,
Kapena moyo wanga pamodzi ndi anthu okhetsa mwazi:
10Amene m'manja mwao muli mphulupulu,
Ndi dzanja lao lamanja ladzala ndi zokometsera mlandu.
11Koma ine, ndidzayenda m'ungwiro wanga;
Mundiombole, ndipo ndicitireni cifundo.
12Phazi langa liponda pacidikha:
M'masonkhano ndidzalemekeza Yehova.

Davide atamadi Yehova, naliradi kuyanjana ndi Mulungu

Salmo la Davide,

1Yehova ndiye kuunika kwanga ndi cipulumutso canga; ndidzaopa yani?
Yehova ndiye mphamvu ya moyo wanga; ndidzacita mantha ndi yani?
2Pondifika ine ocita zoipa kudzadya mnofu wanga,
Inde akundisautsa ndi adani anga, anakhumudwa iwo nagwa.
3Lingakhale gulu la ankhondo limanga misasa kuti andithyole,
Mtima wanga sungacite mantha:
Ingakhale nkhondo ikandiukira,
Nde pomweponso ndidzakhulupira,
4Cinthu cimodzi ndinacipempha kwa Yehova, ndidzacilondola ici:
Kuti ndikhalitse m'nyumba ya Yehova masiku onse a moyo wanga,
Kupenya kukongola kwace kwa Yehova ndi kufunsitsa m'Kacisi wace.
5Cifukwa kuti pa dzuwa la tsoka Iye adzandibisa mumsasa mwace:
Adzandibisa m'tsenjezi mwa cihema cace;
Pathanthwe adzandikweza.
6Ndipo tsopano mutu wanga udzakwezeka pamwamba pa adani anga akundizinga;
Ndipo ndidzapereka m'cihema mwace nsembe za kupfuula mokondwera;
Ndidzayimba, inde, ndidzayimbira Yehova zomlemekeza.
7Imvani, Yehova, liu langa popfuula ine:
Mundicitirenso cifundo ndipo mundibvomereze.
8Pamene munati, Punani nkhope yanga; mtima wanga unati kwa Inu:
Nkhope yanu, Yehova, ndidzaifuna.
9Musandibisire ine nkhope yanu;
Musacotse kapolo wanu ndi kukwiya:
Inu munakhala thandizo langa;
Musanditaye, ndipo musandisiye Mulungu wa cipulumutso canga,
10Pakuti wandisiya atate wanga ndi amai wanga,
Koma Yehova anditola.
11Mundiphunzitse njira yanu, Yehova,
Munditsogolere pa njira yacidikha,
Cifukwa ca adani anga,
12Musandipereke ku cifuniro ca akundisautsa;
Cifukwa zinandiukira mboni zonama ndi iwo akupumira zaciwawa.
13Ndikadapanda kukhulupirira kuti ndikaone ubwino wa Yehova
M'dziko la amoyo, ndikadatanil
14Yembekeza Yehova:

Limbika, ndipo Iye adzalimbitsa mtima wako;
Inde, yembekeza Yehova.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 28

Apempha cipulumutso, ayamika populumutsidwa

Salmo la Davide.

1Kwa Inu, Yehova, ndidzapfuulira;
Thanthwe langa, musandikhalire ngati wosamva:
Pakuti ngati munditontholera ine,
Ndidzafanana nao iwo akutsikira kumanda.
2Mverani mau a kupemba kwanga, pamene ndilirira Inu,
Pamene ndikweza manja anga kuloza ponenera panu poyera.
3Musandikoke kundicotsa pamodzi ndi oipa,
Ndi ocita zopanda pace;
Amene alankhula zamtendere ndi anansi ao,
Koma mumtima mwao muli coipa.
4Muwapatse monga mwa nchito zao, ndi monga mwa coipa cocita iwo:
Muwapatse monga mwa macitidwe a manja ao;
Muwabwezere zoyenera iwo.
5Pakuti sasamala nchito za Yehova,
Kapena macitidwe a manja ace,
Adzawapasula, osawamanganso.
6Wodalitsika Yehova,
Pakuti adamva mau a kupemba kwanga.
7Yehova ndiye mphamvu yanga, ndi cikopa canga;
Mtima wanga wakhulupirira Iye, ndipo anandithandiza:
Cifukwa cace mtima wanga ukondwera kwakukuru;
Ndipo ndidzamyamika nayo Nyimbo yanga.
8Yehova ndiye mphamvu yao,
Inde mphamvu ya cipulumutso ca wodzozedwa wace.
9Pulumutsani anthu anu, ndi kudalitsa colandira canu:
Muwawetenso, ndi kuwanyamula nthawi zonse.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 29

Acenjeza akuru alemekeze Mulungu

Salmo la Davide.

1Perekani kwa Yehova, inu ana a amphamvu,
Perekani kwa Yehova ulemerero ndi mphamvu.
2Perekani kwa Yehova ulemerero wa dzina lace:
Gwadirani Yehova moyera ndi mokometsetsa.
3Liu la Yehova liri pamadzi;
Mulungu wa ulemerero agunda,
Ndiye Yehova pa madzi ambiri.
4Liu la Yehova ndi lamphamvu;
Liu la Yehova ndi lalikurukuru.
5Liu la Yehova lithyola mitengo yamkungudza;
Inde Yehova athyola mikungudza ya ku Lebano.
6Aitumphitsa monga mwana wa ng'ombe;
Lebano ndi Sirio monga msona wa njati.
7Liu la Yehova ligawa malawi a moto.
8Liu la Yehova ligwedeza cipululu;
Yehova agwedeza cipululu ca Kadese.
9Liu la Yehova liswetsa nyama zazikazi,
Ndipo lipulula nkhalango:
Ndipo m'Kacisi mwace zonse ziri m'mwemo zimati, Ulemerero:
10Yehova anakhala pa Cigumula:
Inde Yehova akhala mfumu ku nthawi yomka muyaya.
11Yehova adzapatsa anthu ace mphamvu:
Yehova adzadalitsa anthu ace ndi mtendere.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Mkwiyo wa Mulungu ukhala kanthawi, kuyanja kwao ndi kosatha

Salmo la Davide. Nyimbo yakuperekera nyumba kwa Mulungu.

1Ndidzakukwezani, Yehova; pakuti mwandinyamutsa,
Ndipo simunandikondwetsera adani anga,
2Yehova, Mulungu wanga,
Ndinapfuulira kwa Inu, ndipo munandiciritsa.
3Yehova munabweza moyo wanga kumanda:
Munandisunga ndi moyo, kuti ndingatsikire kudzenje.
4Yimbirani Yehova, inu okondedwa ace,
Ndipo yamikani pokumbukila ciyero cace.
5Pakuti mkwiyo wace ukhala kanthawi kokha;
Koma kuyanja kwace moyo wonse:
Kulira kucezera,
Koma mamawa kuli kupfuula kukondwera.
6Ndipo ine, ndinanena m'phindu langa,
Sindidzagwedezeka nthawi zonse.
7Inu, Yehova, munakhazikitsa phiri langa ndi kuyanja kwanu:
Munabisa nkhope yanu; ndinaopa.
8Ndinapfuulira kwa Inu, Yehova;
Kwa Yehova ndinapemba:
9M'mwazi mwanga muli phindu lanji, potsikira ine kudzenje?
Ngati pfumbi lidzayamika Inu? ngati lidzalalikira coonadi canu?
10Mverani, Yehova, ndipo ndicitireni cifundo:
Yehova, mundithandize ndi Inu.
11Munasanduliza kulira kwanga kukhale kusekera;
Munandibvula ciguduli canga, ndipo munandibveka cikondwero:
12Kuti ulemu wanga uyimbire Inu, wosakhala cete.
Yehova Mulungu wanga, ndidzakuyamikani nthawi zonse.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 31

Davide apempha kolimba Mulungu amlanditse, natama cifundo cao, nauzitsa anthu a Mulungu amtame

Kwa Mkulu wa Nyimbo. Salmo la Davide.

1Ndakhulupirira Inu, Yehova, ndikhale wopanda manyazi nthawi zonse:
Mwa cilungamo canu ndipulumutseni ine.
2Mundicherere khutu lanu; ndipulumutseni msanga:
Mundikhalire ine thanthwe lolimba, nyumba yamalinga yakundisunga.
3Pakuti Inu ndinu thanthwe langa ndi linga langa;
Ndipo cifukwa ca dzina lanu ndiyendetseni bwino, ndipo nditsogolereni.
4Mundionjole m'ukonde umene anandichera mobisika.
Pakuti Inu ndinu mphamvu yanga.
5Ndipereka mzimu wanga m'dzanja lanu:
Mwandiombola, Inu Yehova, Mulungu wa coonadi.
6Ndikwiya nao iwo akusamala zacabe zonama:
Koma ndikhulupirira Yehova.
7Ndidzakondwera ndi kusangalala m'cifundo canu:
Pakuti mudapenya zunzo langa;
Ndipo mudadziwa mzimu wanga mu nsautso yanga:
8Ndipo simunandipereka m'dzanja la mdani;
Munapondetsa mapazi anga pali malo.
9Mundicitire cifundo, Yehova, pakuti ndasautsika ine:
Diso langa, mzimu wanga, ndi mimba yanga, zapuwala ndi mabvuto,
10Pakuti moyo wanga watha ndi cisoni, ndi zaka zanga zatha ndi kuusa moyo:
Mphamvu yanga yafoka cifukwa ca kusakaza kwanga, ndi mafupa anga apuwala.
11Ndakhala cotonza cifukwa ca akundisautsa onse,
Inde, koposa kwa anansi anga; ndipo anzanga andiyesa coopsa:
Iwo akundipenya pabwalo anandithawa.
12Ndaiwalika m'mtima monga wakufa:
Ndikhala monga cotengera cosweka.
13Pakuti ndamva ugogodi wa ambiri,
Mantha andizinga:
Pondipangira ciwembu,
Anatsimikiza mtima kulanda moyo wanga.
14Koma ine ndakhulupirira Inu, Yehova:
Ndinati, Inu ndinu Mulungu wanga,
15Nyengo zanga ziri m'manja mwanu:

Mundilanditse m'manja a adani anga, ndi kwa iwo akundilondola ine.
16Walitsani nkhope yanu pa mtumiki wanu:
Mundipulumutse ndi cifundo canu.
17Yehova, musandicititse manyazi; pakuti ndapfuulira kwa Inu:
Oipa acite manyazi, atonthole m'manda.
18Ikhale yosalankhula milomo ya mabodza,
Imene imalankhula mwacipongwe pa olungama mtima,
Ndi kudzikuza ndi kunyoza.
19Ha! kukoma kwanu ndiko kwakukuru nanga, kumene munasungira iwo akuopa Inu,
Kumene munacitira iwo akukhulupirira Inu, pamaso pa ana a anthu!
20Pobisalira pamaso panu mudzawabisa kwa ciwembu ca munthu:
Mudzawabisa iwo mumsasa kuti muwalanditse pa kutetana kwa malilime.
21Wolemekezeka Yehova:
Pakuti anandicitira cifundo cace codabwiza m'mudzi walinga.
22Ndipo ine, pakutenga nkhawa, ndinati, Ndadulidwa kundicotsa pamaso panu:
Komatu munamva mau a kupemba kwanga pamene ndinapfuulira kwa Inu.
23Kondani Yehova, Inu nonse okondedwa ace:
Yehova asunga okhulupirika,
Ndipo abwezera zocuruka iye wakucita zodzitama.
24Limbikani, ndipo Iye adzalimbitsa mtima wanu,
Inu nonse akuyembekeza Yehova.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 32

Mwai wa munthu amene Mulungu wamkhululukira

Cilangizo ca Davide.

1Wodala munthuyo wokhululukidwa chimo lace;
Wokwiriridwa coipa cace.
2Wodala munthuyu Yehova samwerengera mphulupulu zace;
Ndimo mumzimu mwace mulibe cinyengo.
3Pamene ndinakhala cete mafupa anga anakalamba
Ndi kubuula kwanga tsiku lonse.
4Cifukwa usana ndi usiku dzanja lanu linandilemera ine;
Uwisi wanga unasandulika kuuma kwa malimwe.
5Ndinabvomera coipa canga kwa Inu;
Ndipo mphulupulu yanga sindinaibisa.
Ndinati, Ndidzaululira Yehova macimo anga;
Ndipo munakhululukira coipa ca kulakwa kwanga.
6Cifukwa cace oyera mtima onse apemphere kwa Inu,
Pa nthawi ya kupeza Inu:
Indetu pakusefuka madzi akuru
Sadzamfikira iye.
7Inu ndinu mobisalira mwanga; M'nsautso mudzandisunga;
Mudzandizinga ndi Nyimbo za cipulumutso.
8Ine ndidzakulangiza ndi kuphunzitsa iwe za njira ukayendayo;
Ndidzakupangira ndi diso langa lakuyang'ana iwe.
9Musakhale monga kavalo, kapena ngati buru, wopanda nzeru:
Zomangira zao ndizo cam'kamwa ndi capamutu zakuwakokera,
Pakuti ukapanda kutero sadzakuyandikiza.
10Zisoni zambiri zigwera woipa:
Koma cifundo cidzamzinga iye wakukhulupirira Yehova.
11Sekerani mwa Yehova, ndimo kondwerani inu olungama mtima;
Ndipo pfuulani mokondwera nonsenu oongoka mtima.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 33

Alemekeza Mulungu wolenga, wosunga zonse

1Pfuulani mokondwera mwa Yehova, inu olungama mtima:
Oongoka mtima ayenera kulemekeza.
2Yamikani Yehova ndi zeze:
Myimbireni ndi cisakasa ca zingwe khumi.
3Mumyimbire Iye Nyimbo yatsopano;
Muyimbe mwaluso kumveketsa mau.
4Pakuti mau a Yehova ali olunjika;
Ndi nchito zace zonse zikhulupirika.
5Iye ndiye wakukonda cilungamo ndi ciweruzo:
Dziko lapansi ladzala ndi cifundo ca Yehova.
6Zakumwamba zinalengedwa ndi mau a Yehova;
Ndipo ndi mpweya wa m'kamwa mwace khamu lao lonse.
7Amaunjika madzi a m'nyanja monga mulu:
Amakundika zakudya mosungiramo.
8Dziko lonse lapansi liope Yehova:
Ponse pali anthu acite mantha cifukwa ca Iye,
9Pakuti ananena, ndipo cinacitidwa;
Analamulira, ndipo cinakhazikika.
10Yehova aphwanya upo wa amitundu:
Asandutsa cabe zolingirira za mitundu ya anthu.
11Ciweruzo ca Yehova cikhazikika cikhazikikire,
Zolingirira za m'mtima mwace ku mibadwo mibadwo.
12Wodalitsika mtundu wa anthu umene Yehova ndiye Mulungu wao;
Mtundu womwe anausankha ukhale colandira ca iye yekha.
13Yehova apenyerera m'mwamba; Aona ana onse a anthu.
14M'malo akhalamo Iye, amapenya pansi
Pa onse akukhala m'dziko lapansi;
15Iye amene akonza mitima ya iwo onse,
Amene azindikira zocita zao zonse.
16Palibe mfumu yoti gulu lalikuru limpulumutsa:
Mphamvu yaikuru siicilanditsa ciphona,
17Kavalo safikana kupulumuka naye:
Cinkana mphamvu yace njaikuru sapulumutsa.
18Taonani, diso la Yehova liri pa iwo akumuopa Iye,
Pa iwo akuyembekeza cifundo cace;
19Kupulumutsa moyo wao kwa imfa,
Ndi kuwasunga ndi moyo m'nyengo ya njala.
20Moyo wathu walindira Yehova:
Iye ndiye thandizo lathu ndi cikopa cathu.
21Pakuti mtima wathu udzakondwera mwa Iye,
Cifukwa takhulupirira dzina lace loyera.
22Yehova, cifundo canu cikhale pa ife,

Monga takuyembekezani Inu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 34

Davide alemekeza Yehova womlanditsa, nafulumiza ena amtame

Salimo la Davide. Muja anasintha makhalidwe ace pamaso pa Abimeleke, amene anampitikitsa ndipo anacoka.

1Ndidzalemekeza Yehova nyengo zonse;
Kumlemekeza kwace kudzakhala m'kamwa mwanga kosalekeza.
2Moyo wanga udzatamanda Yehova;
Ofatsa adzakumva nadzakondwera.
3Bukitsani pamodzi ndine ukuru wa Yehova,
Ndipo tikweze dzina lace pamodzi.
4Ndinafuna Yehova ndipo anandibvomera,
Nandlianditsa m'mantha anga Onse.
5Iwo anayang'ana Iye nasanguruka;
Ndipo pankhope pao sipadzacita manyazi,
6Munthu uyu wozunzika anapfuula, ndipo Yehova anamumva,
Nampulumutsa m'masautso ace onse.
7Mngelo wa Yehova azinga kuwacinjiriza iwo akuopa Iye,
Nawalanditsa iwo.
8Talawani, ndipo onani kuti Yehova ndiye wabwino;
Wodala munthuyo wakukhulupirira Iye.
9Opani Yehova, inu oyera mtima ace;
Cifukwa iwo akumuopa Iye sasowa.
10Misona ya mkango isowa nimva njala:
Koma iwo akufuna Yehova sadzasowa kanthu kabwino.
11Idzani ananu ndimvereni ine:
Ndidzakulangizani zakumuopa Yehova.
12Munthu wokhumba moyo ndani,
Wokonda masiku, kuti aone zabwino?
13Uletse lilime lako lisachule zoipa,
Ndipo milomo yako isalankhule cinyengo.
14Pfutuka pazoipa, nucite zabwino,
Funa mtendere ndi kuulondola.
15Maso a Yehova ali pa olungama mtima,
Ndipo makutu ace achereza kulira kwao.
16Nkhopeya Yehovaitsutsananao akucita zoipa,
Kudula cikumbukilo cao pa dziko lapansi.
17Iwowo anaitana, ndipo Yehova anawamva,
Nawalanditsa ku masautso ao onse.
18Yehova ali pafupi ndi iwo a mtimawosweka,
Apulumutsa iwo a mzimu wolapadi,
19Masautso a wolungama mtima acuruka:
Koma Yehova amlanditsa mwa onsewa.
20Iye asunga mafupa ace onse:

Silinatyoka limodzi lonse.
21Mphulupulu idzamupha woipa:
Ndipo adzawatsutsa kumlandu iwo akudana naye wolungama.
22Yehova aombola moyo wa anyamata ace,
Ndipo sadzawatsutsa kumlandu onse akukhulupirira Iye.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 35

Davide apempha Mulungu alange otpa

Salmo la Davide,

1Tsutsanani nao iwo akutsutsana nane, Yehova:
Limbanani nao iwo akulimbana nane.
2Gwirani cikopa cocinjiriza, Ukani kundithandiza.
3Sololani nthungo, ndipo muwatsekerezere kunjira akundilondola:
Nenani ndi moyo wanga, Cipulumutso cako ndine.
4Athe nzeru nacite manyazi iwo akufuna moyo wanga:
Abwezedwe m'mbuyo nasokonezeke iwo akundipangira ciwembu.
5Akhale monga mungu kumphepo,
Ndipo mngelo wa Yehova awapitikitse.
6Njira yao ikhale ya mdima ndi yoterera,
Ndipo mngelo wa Yehova awalondole.
7Pakuti anandichera ukonde wao m'mbunamo kopanda cifukwa,
Anakumbira moyo wanga dzenje kopanda cifukwa.
8Cimgwere modzidzimutsa cionongeko;
Ndipo ukonde wace umene anaucha umkole yekha mwini:
Agwemo, naonongeke m'mwemo.
9Ndipo moyo wanga udzakondwera mwa Yehova:
Udzasekera mwa cipulumutso cace.
10Mafupa anga onse adzanena, Yehova, afanana ndi Inu ndani,
Wakulanditsa wozunzika kwa iye amene amposa mphamvu,
Ndi wozunzika ndi waumphawi kwa iye amfunkhira?
11Mboni za ciwawa ziuka,
Zindifunsa zosadziwa ine.
12Andibwezera coipa m'malo mwa cokoma,
Inde, asaukitsa moyo wanga.
13Koma ine, pakudwala iwowa, cobvala canga ndi ciguduli:
Ndinazunza moyo wanga ndi kusala;
Ndipo pemphero langa linabwera ku cifuwa canga.
14Ndakhala ine monga ngad iye anali bwenzi langa, kapena mbale wanga:
Polira ndinaweramira pansi, monga munthu wakulira maliro amai wace.
15Ndipo pakutsimphina ine anakondwera, nasonkhana pamodzi:
Akundipanda anandisonkhanira; ndipo sindinacidziwa:
Anandingamba osaleka:
16Pakati pa onyodola pamadyerero,
Anandikukutira mano.
17Ambuye, mudzapenyerabe nthawi yanji?
Bwezani moyo wanga kwa zakundiononga zao,
Wanga wa wokha kwa misona ya mkango.
18Ndidzakuyamikanimumsonkhano waukuru:

M'cikhamu ca anthu ndidzakulemekezani.
19Adani anga asandikondwerere ine monyenga;
Okwiya nane kopanda cifukwa asanditsinzinire.
20Pakuti salankhula zamtendere:
Koma apangira ciwembu odekha m'dziko.
21Ndipo andiyasamira m'kamwa mwao;
Nati, Hede, Hede, diso lathu lidacipenya.
22Yehova, mudacipenya; musakhale cete:
Ambuye, musakhale kutali ndi ine.
23Galamukani, ndipo khalani maso kundiweruzira mlandu wanga,
Mulungu wanga ndi Ambuye wanga,
24Mundiweruze monga mwa cilungamo canu, Yehova Mulungu wanga;
Ndipo asandisekerere ine.
25Asanene mumtima mwao, Hede, momwemo!
Asanene, Tammeza iye.
26Acite manyazi, nadodome iwo akukondwera cifukwa ca coipa cidandigwera:
Abvekeke ndi manyazi ndi kupunzika iwo akudzikuza pa ine.
27Apfuule mokondwera nasangalale iwo akukondwera naco cilungamo canga:
Ndipo anene kosalekeza, Abuke Yehova,
Amene akondwera ndi mtendere wa mtumiki wace.
28Ndipo lilime langa lilalikire cilungamo canu,
Ndi lemekezo lanu tsiku lonse.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 36

Kuipitsitsa kwa anthu, kukometsetsa kwa Mulungu

Kwa Mkulu wa Nyimbo. Salimo la Davide, mtumiki wa Yehova.

1Colakwa ca woipayo cimati m'kati mwa mtima wanga,
Palibe kuopa Mulungu pamaso pace.
2Pakud adzidyoletsa yekha m'kuona kwace,
Kuti anthu sadzacipeza coipa cace ndi kukwiya naco.
3Mau a pakamwa pace ndiwo opanda pace ndi onyenga:
Waleka kuzindikira ndi kucita bwino.
4Alingirira zopanda pace pakama pace;
Adziika panjira posad pabwino;
Coipa saipidwa naco.
5Yehova, m'mwambamuli cifundo canu;
Coonadi canu cifikira kuthambo.
6Cilungamo canu cikunga mapiri a Mulungu;
Maweruzo anu akunga cozama cacikuru:
Yehova, musunga munthu ndi nyama.
7Ha! cifundo canu, Mulungu, ncokondedwadi!
Ndipo ana a anthu athawira ku mthunzi wa mapiko anu.
8Adzakhuta kwambiri ndi zonona za m'nyumba mwanu:
Ndipo mudzawamwetsa mu mtsinje wa zokondweretsa zanu.
9Pakuti citsime ca moyo ciri ndi Inu:
M'kuunika kwanu tidzaona kuunika.
10Tanimphitsani cifundo canu pa iwo akudziwa Inu;
Ndi cilungamo canu pa oongoka mtima.
11Phazi la akudzikuza lisandifikire ine,
Ndi dzanja la oipa lisandicotse.
12Pomwepo padagwera ocita zopanda pace:
Anawalikha, ndipo sadzatha kuukanso.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Kusangalala kwa ocimwa kudzatha, olungama akhalitsa nathandizidwa ndi Mulungu

Salmo la Davide.

1Usabvutike mtima cifukwa ca ocita zoipa,
Usacite nsanje cifukwa ca ocita cosalungama.
2Pakuti adzawamweta msanga monga udzu,
Ndipo adzafota monga msipu wauwisi.
3Khulupirira Yehova, ndipo cita cokoma;
Khala m'dziko, ndipo tsata coonadi.
4Udzikondweretsenso mwa Yehova;
Ndipo iye adzakupatsa zokhumba mtima wako.
5Pereka njira yako kwa Yehova; Khulupiriranso Iye, adzacicita.
6Ndipo adzaonetsa cilungamo cako monga kuunika,
Ndi kuweruza kwako monga usana.
7Khala cete mwa Yehova, numlindirire Iye:
Usabvutike mtima cifukwa ca iye wolemerera m'njira yace,
Cifukwa ca munthu wakucita ciwembu.
8Leka kupsa mtima, nutaye mkwiyo:
Usabvutike mtima ungacite coipa,
9Pakuti ocita zoipa adzadulidwa:
Koma iwo akuyembekeza Yehova, iwowa adzalandira dziko lapansi.
10Katsala kanthawi ndipo woipa adzatha psiti:
Inde, udzayang'anira mbuto yace, nudzapeza palibe.
11Koma ofatsa adzalandira dziko lapansi;
Nadzakondwera nao mtendere wocuruka.
12Woipa apangira ciwembu wolungama,
Namkukutira mano.
13Ambuye adzamseka:
Popeza apenya kuti tsiku lace likudza.
14Oipa anasolola lupanga, nakoka uta wao;
Alikhe ozunzika ndi aumphawi,
Aphe amene ali oongoka m'njira:
15Lupanga lao lidzalowa m'mtima mwao momwe,
Ndipo mauta ao adzatyoledwa.
16Zocepa zace za wolungama zikoma
Koposa kucuruka kwao kwa oipa ambiri.
17Pakuti manja a oipa adzatyoledwa:
Koma Yehova acirikiza olungama.
18Yehova adziwa masiku a anthu angwiro:
Ndipo cosiyira cao cidzakhala cosatha.
19Sadzacita manyazi m'nyengo yoipa:
Ndipo m'masiku a njala adzakhuta.
20Pakuti oipa adzatayika,

Ndipo adani ace a Yehova adzanga mafuta a ana a nkhosa:
Adzanyeka, monga utsi adzakanganuka.
21Woipa akongola, wosabweza:
Koma wolungama acitira cifundo, napereka.
22Pakuti iwo amene awadalitsa adzalandira dziko lapansi;
Koma iwo amene awatemberera adzadulidwa.
23Yehova akhazikitsa mayendedwe a munthu;
Ndipo akondwera nayo njira yace.
24Angakhale akagwa, satayikiratu:
Pakuti Yehova agwira dzanja lace.
25Ndinali mwana ndipo ndakalamba:
Ndipo sindinapenya wolungama wasiyidwa,
Kapena mbumba zace zirinkupempha cakudya.
26Tsiku lonse acitira cifundo, nakongoletsa;
Ndipo mbumba zace zidalitsidwa.
27Siyana naco coipa, nucite cokoma,
Nukhale nthawi zonse.
28Pakuti Yehova akonda ciweruzo,
Ndipo sataya okondedwa ace:
Asungika kosatha:
Koma adzadula mbumba za oipa.
29Olungama adzalandira dziko lapansi,
Nadzakhala momwemo kosatha.
30Pakamwa pa wolungama palankhula zanzeru,
Ndi lilime lace linena ciweruzo.
31Malamulo a Mulungu wace ali mumtima mwace;
Pakuyenda pace sadzaterereka.
32Woipa aunguza wolungama,
Nafuna kumupha.
33Yehova sadzamsiya m'dzanja lace:
Ndipo sadzamtsutsa poweruzidwa iye.
34Yembekeza Yehova, nusunge njira yace,
Ndipo Iye adzakukweza kuti ulandire dziko:
Pakudutidwa oipa udzapenya,
35Ndapenya woipa, alikuopsa,
Natasa monga mtengo wauwisi wanzika.
36Koma anapita ndipo taona, kwati zi:
Ndipo ndinampwaira osampeza.
37Tapenya wangwiro, ndipo taona woongoka mtima!
Pakuti ku matsiriziro ace a munthuyo kuti mtendere.
38Koma olakwa adzaonongeka pamodzi:
Matsiriziro a oipa adzadutidwa.
39Koma cipulumutso ca olungama cidzera kwa Yehova,
Iye ndiye mphamvu yao m'nyengo ya nsautso.

40Ndipo Yehova awathandiza, nawalanditsa:
Awalanditsa kwa oipa nawapulumutsa,
Cifukwa kuti anamkhulupirira Iye,

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 38

Davide aulula zoipa zace, apempha Mulungu amkhululukire namthandize

Salmo la Davtde, lakukumbutsa.

1Yehova, musandidzudzule ndi mkwiyo wanu:
Ndipo musandilange moopsa m'mtima mwanu.
2Pakuti mibvi yanu yandilowa,
Ndi dzanja lanu landigwera.
3Mumnofu mwanga mulibe camoyo cifukwa ca ukali wanu;
Ndipo m'mafupa anga simuzizira, cifukwa ca colakwa canga.
4Pakuti mphulupulu zanga zapitirira pamutu panga:
Ndathodwa nazo monga ndi katundu wolemera.
5Mabala anga anunkha, adaola, Cifukwa ca kupusa kwanga.
6Ndapindika, ndawerama kwakukuru;
Ndimayenda woliralira tsiku lonse.
7Pakuti m'cuuno mwanga mutentha kwambiri;
Palibe pamoyo m'mnofu mwanga,
8Ndafoka ine, ndipo ndacinjizidwa:
Ndabangula cifukwa ca kumyuka mtima wanga.
9Ambuye, cikhumbo canga conse ciri pamaso panu;
Ndipo kubuula kwanga sikubisika kwa Inu.
10Mtima wanga ugundagunda, mphamvu yanga yacoka:
Ndipo kuunika kwa maso anga, ndi iko komwe kwandicokera.
11Ondikonda ndi anzanga apewa mliri wanga;
Ndipo anansi anga aima patali.
12Ndipo andichera misampha iwo akufuna moyo wanga;
Ndipo iwo akuyesa kundicitira coipa alankhula zoononga,
Nalingirira zonyenga tsiku lonse.
13Koma ine, monga gonthi, sindimva;
Ndipo monga munthu wosalankhula, sinditsegula pakamwa panga.
14Inde ndikunga munthu wosamva,
Ndipo m'kamwa mwanga mulibe makani.
15Pakuti ndikuyembekezani Inu, Yehova;
Inu mudzayankha, Ambuye Mulungu wanga.
16Pakuti ndinati, Asakondwerere ine:
Pakuterereka phazi langa, asadzikuze pa ine.
17Ndafikana potsimphina;
Ndipo cisoni canga ciri pamaso panga cikhalire.
18Pakuti ndidzafotokozera mphulupulu yanga;
Nditenga nkhawa cifukwa ca chimo langa.
19Koma adani anga ali ndi moyo, nakhalandi mphamvu:
Ndipo akundida kopanda cifukwa acuruka.
20Ndipo iwo akubwezera coipa pa cabwino
Atsutsana nane, popeza nditsata cabwino.

21Musanditaye, Yehova:
Mulungu wanga, musakhale kutali ndi ine.
22Fulumirani kundithandiza,
Ambuye, cipulumutso canga.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Kupepuka kwa moyo uno

Kwa Mkulu wa Nyimbo, kwa Yedutun, Salmo la Davide.

1Ndinati, Ndidzasunga njira zanga,
Kuti ndingacimwe ndi lilime langa:
Ndidzasunga pakamwa panga ndi cam'kamwa,
Pokhala woipa ali pamaso panga.
2Ndinatonthola osanena mau, ndinakhala cete osalawa cokoma;
Ndipo cisoni canga cinabuka.
3Mtima wanga unatentha m'kati mwaine;
Unayaka moto pakulingirira ine:
Pamenepo ndinalankhula ndi lilime langa:
4Yehova, mundidziwitse cimariziro canga,
Ndi mawerengedwe a masiku anga ndi angati;
Ndidziwe malekezero anga,
5Onani, munaika masiku anga akhale monga kuyesa dzanja;
Ndipo zaka zanga ziri ngati cabe pamaso panu:
Indedi munthu ali yense angakhale wokhazikika, ali cabe konse.
6Indedi munthu ayenda ngati mthunzi:
Indedi abvutika cabe:
Asonkhanitsa cuma, ndipo sadziwa adzacilandira ndani?
7Ndipo tsopano, Ambuye, ndilindira ciani?
Ciyembekezo canga ciri pa Inu.
8Ndipulumutseni kwa zolakwa zangazonse:
Musandiike ndikhale cotonza ca wopusa.
9Ndinakhala du, sindinatsegula pakamwa panga;
Cifukwa inu mudacicita.
10Mundicotsere cobvutitsa canu;
Pandithera ine cifukwa ca kulanga kwa dzanja lanu.
11Pamene mulanga munthu ndi zomdzudzula cifukwa ca mphulupulu,
Mukanganula kukongola kwace monga mumacita ndi kadzoce:
Indedi, munthu ali yense ali cabe.
12Imvani pemphero langa, Yehova, ndipo cherani khutu kulira kwanga;
Musakhale cete pa misozi yanga:
Pakuti ine ndine mlendo ndi Inu,
Wosakhazikika, monga makolo anga onse.
13Ndiloleni, kuti nditsitsimuke,
Ndisanamuke ndi kukhala kuli zi.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 40

Alemekeza cipulumutso ca Mulungu, alalikira poyera cilungamo ca Mulungu

Kwa Mkulu wa Nyimbo. Salmo la Davide.

1Kuyembekeza ndayembekeza Yehova;
Ndipo anandilola, namva kupfuula kwanga.
2Ndipo anandikweza kunditurutsa m'dzenje la citayiko, ndi m'thope la pacithaphwi;
Nandipondetsa pathanthwe, nakhazika mayendedwe anga.
3Ndipo anapatsa Nyimbo yatsopano m'kamwa mwanga, cilemekezo ca kwa Mulungu wanga;
Ambiri adzaciona, nadzaopa,
Ndipo adzakhulupirira Yehova.
4Wodala munthuyo wakuyesa Yehova wokhulupirika;
Wosasamala odzikuza, ndi opatukira kubodza.
5Inu, Yehova, Mulungu wanga, zodabwiza zanu mudazicita nzambiri,
Ndipo zolingirira zanu za pa ife;
Palibe wina wozifotokozera Inu;
Ndikazisimba ndi kuzichula, Zindicurukira kuziwerenga.
6Nsembe ndi copereka simukondwera nazo;
Mwanditsegula makutu:
Nsembe yopsereza ndi yamacimo simunapempha.
7Pamenepo ndinati, Taonani, ndadza;
M'buku mwalembedwa za Ine:
8Kucita cikondwero canu kundikonda, Mulungu wanga;
Ndipo malamulo anu ali m'kati mwamtima mwanga.
9Ndalalikira cilungamo mu msonkano waukuru;
Onani, sindidzaletsa milomo yanga,
Mudziwa ndinu Yehova.
10Cilungamo canu sindinacibisa m'kati mwamtima mwanga;
Cikhulupiriko canu ndi cipulumutso canu ndinacinena;
Cifundo canu ndi coonadi canu sindinacibisira msonkhano waukuru.
11Inu Yehova, simudzandikaniza nsoni zanu:
Cifundo canu ndi coonadi canu zindisunge cisungire.
12Pakuti zoipa zosawerengeka zandizinga,
Zocimwa zanga zandipeza kotero kuti sindikhoza kupenya;
Ziposa tsitsi la mutu wanga, ndipo wandicokera mtima.
13Ndikupemphani, Yehova, ndilanditseni:
Fulumirani kudzandithandiza, Yehova.
14Acite manyazi nadodome
Iwo akulondola moyo wanga kuti auononge:
Abwerere m'mbuyo, nacite manyazi iwo okondwera kundicitira coipa.

15Apululuke, mobwezera manyazi ao
Amene anena nane, Hede, hede.
16Asekerere nakondwerere mwa Inu onse akufuna Inu:
Iwo akukonda cipulumutso canu asaleke kunena, Abuke Yehova.
17Ndipo ine ndine wozunzika ndi waumphawi;
Koma Ambuye andikumbukila ine:
Inu ndinu mthandizi wanga, ndi mpulumutsi wanga:
Musamacedwa, Mulungu wanga,

©The Bible Society of Malawi, 1992

Mulungu adalitsa wosamalira osauka. Adani ndi mabwenzi amcitira Davide zoipa, Mulungu amlanditse

Kwa Mkulu wa Nyimbo. Salmo la Davide.

1 Wodala iye amene asamalira wosauka:
Tsiku la tsoka Yehova adzampulumutsa:
2 Yehova adzamsunga, nadzamsunga ndi moyo, ndipo adzadalitsika pa dziko lapansi;
Ndipo musampereke ku cifuniro ca adani ace.
3 Yehova adzamgwiriziza pa kama wodwalira;
Podwala iye mukonza pogona pace,
4 Ndinati ine, Mundicitire cifundo, Yehova:
Ciritsani mtima wanga; pakuti ndacimwira Inu.
5 Adani anga andinenera coipa, ndi kuti,
Adzafa liti, ndi kutayika dzina lace?
6 Ndipo akadza kundiona wina angonena bodza;
Mumtima mwace adzisonkhera zopanda pace:
Akamka nayenda namakanena:
7 Onse akudana nane andinong'onezerana;
Apangana condiipsa ine.
8 Camgwera cinthu coopsa, ati;
Popeza ali gonire sadzaukanso.
9 Ngakhale bwenzi langa leni leni, amene ndamkhulupirira, ndiye amene adadyako mkate wanga,
Anandikwezera cidendene cace.
10 Koma Inu, Yehova, mundicitire cifundo, ndipo mundiutse,
Kuti ndiwabwezere.
11 Umo ndidziwa kuti mukondwera ndi ine,
Popeza mdani wanga sandiseka.
12 Ndipo ine, mundigwirizize m'ungwiro wanga,
Ndipo mundiike pankhope panu ku nthawi yamuyaya.
13 Wodalitsika Yehova, Mulungu wa Israyeli,
Kucokera nthawi yosayamba kufikira nthawi yosatha.
Amen, ndi Amen.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 42

Mtima wolira kuyanjana ndi Mulungu m'Kacisi

Kwa Mkulu wa Nyimbo. Cilangizo ca kwa ana a Kora.

1Monga nswala ipuma wefuwefu kukhumba mitsinje;
Motero moyo wanga upuma wefuwefu kukhumba Inu, Mulungu.
2Moyo wanga uli ndi ludzu la kwa Mulungu, la kwa Mulungu wamoyo:
Ndikadze liti kuoneka pamaso pa Mulungu?
3Misozi yanga yakhalangati cakudya canga,
Usana ndi usiku;
Pakunena iwo kwa ine dzuwa lonse,
Mulungu wako ali kuti?
4Ndizikumbukila izi ndipo nditsanulira moyo wanga m'kati mwa ine,
Pakuti ndidafopita ndi unyinji wa anthu,
Ndinawatsogolera ku nyumba ya Mulungu, ndi mau akuyimbitsa ndi kuyamika,
Ndi unyinji wakusunga dzuwa lokondwera.
5Udziweramiranji moyo wanga iwe?
Ndi kuzingwa m'kati mwanga?
Yembekeza Mulungu, pakuti ndidzamyamikanso
Cifukwa ca cipulumutso ca nkhope yace.
6Mulungu wanga, moyo wanga
Udziweramira m'kati mwanga;
Cifukwa cace ndikumbukila Inu m'dziko la Yordano,
Ndi mu Ahermone, m'kaphiri ka Mizara.
7Madzi akuya aitanizana ndi madzi akuya,
Pa mkokomo wa matiti anu: Mafunde onse a nyondonyondo anandimiza ine.
8Koma usana Yehova adzalamulira cifundo cace,
Ndipo usiku Nyimbo yace idzakhala ndi ine.
Inde pemphero la kwa Yehova wa moyowanga.
9Ndidzati kwa Mulungu, thanthwe langa, mwandiiwala cifukwa ninji?
Ndimayenderanji wakulira Cifukwa ca kundipsinja mdaniyo?
10Adani anga andinyoza ndi kundityola mafupa anga;
Pakunena ndine dzuwa lonse,
Mulungu wako ali kuti?
11Udziweramiranji moyo wanga iwe?
Ndi kuzingwa m'kati mwanga?
Yembekeza Mulungu: pakuti ndidzamlemekeza tsopanonso,
Ndiye cipulumutso ca nkhope yanga ndi Mulungu wanga,

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 43

Davide alira akhale ku Kacisi

1Mundiweruzire, Mulungu, ndipo mundinenere mlandu kwa anthu
opanda cifundo:
Mundilanditse kwa munthu wonyenga ndi wosalungama.
2Pakuti Inu ndinu Mulungu wa mphamvu yanga; mwanditayiranji?
Ndimayenderanji woliralira cifukwa ca kundipsinja mdani?
3Tumizirani kuunika kwanu ndi coonadi canu zinditsogolere:
Zindifikitse ku phiri lanu loyera,
Kumene mukhala Inuko.
4Kuti ndipite kufikira guwa la nsembe la Mulungu,
Kufikira Mulungu wa cimwemwe canga ceniceni:
Ndi kuti ndikuyamikeni ndi zeze, Mulungu, Mulungu wanga.
5Udziweramiranji moyo wanga iwe?
Ndi kuzingwa m'kati mwanga?
Yembekeza Mulungu: pakuti ndidzamyamikanso,
Ndiye cipulumutso ca nkhope yanga, ndi Mulungu wanga.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 44

Anthu a Mulungu akumbuke zithandizo zakale popempha cipulumutso m'tsoka lao

Kwa Mkulu Wa Nyimbo; Cuangizo ca ana a Kora.

1Mulungu, tidamva m'makutu mwathu, makolo athu anatisimbira,
Za nchitoyo mudaicita masiku ao, masiku akale.
2Inu munapitikitsa amitundu ndi dzanja lanu, koma iwowa munawaoka;
Munasautsa mitundu ya anthu, ndipo munawaingitsa,
3Pakuti sanalanda dziko ndi lupanga lao,
Ndipo mkono wao sunawapulumutsa:
Koma dzanja lanu lamanja, ndi mkono wanu, ndi kuunika kwa nkhope yanu.
Popeza munakondwera nao,
4Inu ndinu mfumu yanga, Mulungu:
Lamulirani cipulumutso ca Yakobo.
5Mwa Inu tidzakankhira pansi otsutsana nafe:
M'dzina lanu tidzapondereza akutiukira ife.
6Pakuti sinditama uta wanga,
Ndipo lupanga langa silingandipulumutse.
7Koma Inu munatipulumutsa kwa iwo akutsutsana nafe,
Ndipo akudana nafe, mudawacititsa manyazi.
8Mwa Mulungu tidzitamanda tsiku lonse,
Ndipo dzina lanu tidzaliyamika kosatha.
9Koma mwatitaya, ndi kutinyazitsa;
Ndipo simuturuka nao makamu a nkhondo athu.
10Mutibwereretsa kuthawa otisautsa:
Ndipo akudana nafe adzifunkhira okha.
11Mwatipereka ngati nkhosa zoyenera kuzidya;
Ndipo mwatibalalitsa mwa amitundu.
12Mugulitsa anthu anu kwacabe,
Ndipo mtengo wace simupindula nao.
13Mutisandutsa cotonza kwa anzathu,
Ndi coseketsa ndi colalatitsa iwo akutizinga.
14Mutiika tikhale onyozeka mwa amitundu,
Ndi kuti anthu atipukusire mitu.
15Tsiku lonse cimpepulo canga cikhala pamaso panga,
Ndipo manyazi a pankhope panga andikuta.
16Cifukwa ca mau a wotonza wocitira mwano;
Cifukwa ca mdani ndi wobwezera cilango,
17Zonsezi zatigwera; koma sitinakuiwalani,
Ndipo sitinacita monyenga m'pangano lanu.
18Mtima wathu sunabwerera m'mbuyo,
Ndipo m'mayendedwe athu sitinapatuka m'njira yanu;

19Mungakhale munatityola mokhala zirombo,
Ndi kutiphimba nao mthunzi wa imfa.
20Tikadaiwala dzina la Mulungu wathu,
Ndi kutambasulira manja athu kwa mulungu wacilendo;
21Mulungu sakadasanthula ici kodi?
Pakuti adziwa zinsinsi za mtima.
22Koma, cifukwa ca Inu, tiphedwa tsiku lonse;
Tiyesedwa ngati nkhosa zakuzipha.
23Galamukani, mugoneranji, Ambuye?
Ukani, musatitaye citayire.
24Mubisiranji nkhope yanu,
Ndi kuiwala kuzunzika ndi kupsinjika kwathu?
25Pakuti moyo wathu waweramira kupfumbi:
Pamimba pathu pakangamira dziko lapansi.
26Ukani, tithandizeni,
Tiomboleni mwa cifundo canu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Nyimbo voyimbira ukwati wa mfumu

Kwa Mkulu wa Nyimbo pa Syosyanim. Cilangizo ca kwa ana a Kora. Nyimbo ya cikondi.

1Mtima wanga usefukira naco cinthu cokoma:
Ndinena zopeka ine za mfumu:
Lilime langa ndilo peni yofulumiza kulemba.
2Inu ndinu wokongola ndithu kuposa ana a anthu;
Anakutsanulirani cisomo pa milomo yanu:
Cifukwa cace Mulungu anakudalitsani kosatha.
3Dzimangireni lupanga lanu m'cuuno mwanu, wamphamvu inu,
Ndi ulemerero wanu ndi ukulu wanu.
4Ndipo pindulani, m'ukulu wanu yendani,
Kaamba ka coonadi ndi cifatso ndi cilungamo:
Ndipo dzanja lanu lidzakuphunzitsani zoopsa.
5Mibvi yanu njakuthwa;
Mitundu ya anthu igwa pansi pa Inu:
Iwalasa mumtima adani a mfumu.
6Mpando wacifumu wanu, Mulungu, ukhala nthawi zonse zamkamuyaya:
Ndodo yacifumu ya ufumu wanu ndiyo ndodo yolunjika.
7Mukonda cilungamo, ndipo mudana naco coipa:
Cifukwa cace Mulungu, ndiye Mulungu wanu, wadzoza inu
Ndi mafuta a cikondwerero kuposa anzanu.
8Zobvala zanu zonse nza mure, ndi khonje, ndi kasya;
M'zinyumba za mfumu zomanga ndi minyanga ya njobvu mwatoruka zoyimba za zingwe zokukondweretsani.
9Mwa omveka anu muli ana akazi amafumu:
Ku dzanja lamanja lanu aima mkazi wa mfumu wobvala golidi wa ku Ofiri.
10Tamvera, mwana wamkaziwe, taona, tachera khutu lako;
Uiwalenso mtundu wako ndi nyumba ya atate wako;
11Potero mfumuyo adzakhumba kukoma kwako:
Pakuti ndiye mbuye wako; ndipo iwe umgwadire iye.
12Ndipo mwana wamkazi wa Turo adzafika nayo mphatso;
Acuma a mwa anthu adzapempha kudziwika nanu.
13Mwana wamkazi wa mfumu ngwa ulemerero wonse m'kati mwa nyumba:
Zobvala zace nza made agolidi.
14Adzamtsogolera kwa mfumu wabvala zamawanga-mawanga:
Anamwali anzace omtsata adzafika nao kwa inu.
15Adzawatsogolera ndi cimwemwe ndi kusekerera:
Adzalowa m'nyumba ya mfumu.
16M'malo mwa makolo ako mudzakhala ana ako,

Udzawaika akhale mafumu m'dziko lonse lapansi.
17Ndidzawakumbutsa dzina lanu m'mibadwo mibadwo:
Cifukwa cace mitundu ya anthu idzayamika Inu ku nthawi za nthawi.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 46

Mulungu ndiye pothawirapo anthu ace

Kwa Mkulu wa Nyimbo; Cilangizo ca kwa ana a Kora. Pa Alamot. Nyimbo.

1Mulungu ndiye pothawirapo pathu ndi mphamvu yathu,
Thandizo lopezekeratu m'masautso.
2Cifukwa cace sitidzacita mantha, lingakhale lisandulika dziko lapansi,
Angakhale mapiri asunthika, nakhala m'kati mwa nyanja;
3Cinkana madzi ace akokoma, nacita thobvu,
Nagwedezeka mapiri ndi kudzala kwace.
4Pali mtsinje, ngalande zace zidzakondweretsa mudzi wa Mulungu.
Malo oyera okhalamo Wam'mwambamwamba,
5Mulungu ali m'kati mwace, sudzasunthika:
Mulungu adzauthandiza mbanda kuca.
6Amitundu anapokosera; maufumu anagwedezeka:
Ananena mau, dziko lapansi linasungunuka.
7Yehova wa makamu ali ndi ife;
Mulungu wa Yakobo ndiye pamsanje pathu.
8Idzani, penyani nchito za Yehova,
Amene acita zopululutsa pa dziko lapansi.
9Aletsa nkhondo ku malekezero adziko lapansi;
Athyola uta, nadula nthungo;
Atentha magareta ndi moto.
10Khalani cete, ndipo dziwani kuti Ine ndine Mulungu:
Ndidzabuka mwa amitundu,
Ndidzabuka pa dziko lapansi.
11Yehova wa makamu ali ndi ife,
Mulungu wa Yakobo ndiye pamsanje pathu,

©The Bible Society of Malawi, 1992

Mau a kulemekeza Mulungu mwini dziko lonse lapansi

Kwa Mkulu wa Nyimbo. Salmo la ana a Koro.

1Ombani m'manja, mitundu yonse ya anthu;
Pfuulirani kwa Mulungu ndi liu la kuyimbitsa.
2Pakuti Yehova Wam'mwambamwamba ndiye woopsa;
Ndiye mfumu yaikuru pa dziko lonse lapansi.
3Atigonjetsera anthu,
Naika amitundu pansi pa mapazi athu.
4Atisankhira colowa cathu,
Cokometsetsa ca Yakobo amene anamkonda.
5Mulungu wakwera ndi mpfuu,
Yehova ndi liu la lipenga.
6Yimbirani Mulungu, yimbirani;
Yimbirani Mfumu yathu, yimbirani.
7Pakuti Mulungu ndiye Mfumu ya dziko lonse lapansi;
Yimbirani ndi cilangizo.
8Mulungu ndiye Mfumu ya amitundu:
Mulungu akhala pa mpando wacifumu wace woyera.
9Akulu a anthu asonkhana
Akhale anthu a Mulungu wa Abrahamu:
Pakuti zikopa za dziko lapansi nza Mulungu;
Akwezeka kwakukuru lyeyo.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 48

Ukoma ndi ulemerero wa Ziyoni

Nyimbo; Salmo la ana a Kora.

1Yehova ndiye wamkulu, ayenera kulemekezekadi,
M'mudzi wa Mulungu wathu, m'phiri lace loyera.
2Phiri la Ziyoni, cikhalidwe cace ncokoma
Ku mbali zace za kumpoto,
Ndilo cimwemwe ca dziko lonse lapansi,
Mudzi wa mfumu yaikuru.
3Mulungu adziwika m'zinyumba zace ngati msanje.
4Pakuti, taonani, mafumuwo anasonkhana,
Anapitira pamodzi.
5Anapenya mudziwo, ndipo pamenepo anadabwa;
Anaopsedwa, nathawako.
6Pomwepo anagwidwa nako kunthunthumira;
Anamva cowawa, ngati wam'cikuta.
7Muswa zombo za ku Tarisi ndi mphepo ya kum'mawa.
8Monga tidamva, momwemo tidapenya
M'mudzi wa Yehova wa makamu, m'mudzi wa Mulungu wathu:
Mulungu adzaukhazikitsa ku nthawi yamuyaya.
9Tidalingalira za cifundo canu, Mulungu,
M'kati mwa Kacisi wanu.
10Monga dzina lanu, Mulungu,
Momwemo lemekezo lanu ku malekezero a dziko lapansi:
M'dzanja lamanja lanu mudzala cilungamo.
11Likondwere phiri la Ziyoni,
Asekere ana akazi a Yuda,
Cifukwa ca maweruzo anu.
12Zungulirani Ziyoni, ndipo muuzinge;
Werengani nsanja zace.
13Penyetsetsani malinga ace,
Yesetsani zinyumba zace;
Kuti mukaziwerengere mibadwo ikudza m'mbuyo.
14Pakuti Mulungu ameneyo ndiye Mulungu wathu ku nthawi za nthawi:
Adzatitsogolera kufikira imfa.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 49

Za pansi pano nza cabe

Kwa Mkulu wa Nyimbo; Salmo la ana a Kora.

1Dzamveni kuno, anthu inu nonse;
Cherani khutu, inu nonse amakono,
2Awamba ndi omveka omwe,
Acuma ndi aumphawi omwe.
3Pakamwa panga padzanena zanzeru;
Ndipo cilingiriro ca mtima wanga cidzakhala ca cidziwitso.
4Ndidzachera khutu kufanizo:
Ndidzafotokozera cophiphiritsa canga poyimbira.
5Ndidzaoperanji masiku oipa,
Pondizinga amphulupulu onditsata kucidendene?
6Iwo akutama kulemera kwao;
Nadzitamandira pa kucuruka kwa cuma cao;
7Kuombola mbale sangadzamuombole,
Kapena kumperekera dipo kwa Mulungu:
8(Popeza ciombolo ca moyo wao nca mtengo wace wapatali,
Ndipo cilekeke nthawi zonse)
9Kuti akhale ndi moyo osafa,
Osaona cibvundi.
10Pakuti aona anzeru amafa,
Monga aonongekera wopusa, wodyerera momwemo,
Nasiyira ena cuma cao.
11Mumtima mwao ayesa kuti nyumba zao zikhala cikhalire,
Ndi mokhala iwo ku mibadwo mibadwo;
Achapo dzina lao padziko pao.
12Koma munthu wa ulemu wace sakhalitsa:
Afanana ndi nyama za kuthengo, afanana nazo.
13Njira yao yino ndiyo kupusa kwao:
Koma akudza m'mbuyo abvomereza mau ao.
14Aikidwa m'manda ngati nkhosa;
Mbusa wao ndi imfa:
Ndipo m'mawa mwace oongoka mtima adzakhala mafumu ao;
Ndipo maonekedwe ao adzanyekera kumanda, kuti pokhala pace padzasowa.
15Koma Mulungu adzaombola moyo wanga ku mphamvu ya manda:
Pakuti adzandilandira ine.
16Usaope polemezedwa munthu,
Pocuruka ulemu wa nyumba yace;
17Pakuti pomwalira iye sadzamuka nako kanthu kali konse;
Ulemu wace sutsika naye kumtsata m'mbuyo.
18Angakhale anadalitsa moyo wace pokhala ndi moyo,
Ndipo anthu akulemekeza iwe, podzicitira wekha zokoma,

19 Adzamuka ku mbadwo wa makolo ace;
Sadzaona kuunika nthawi zonse.
20 Munthu waulemu, koma wosadziwitsa,
Afanana ndi nyama za kuthengo, afanana nazo.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Mulungu woweruza wa dziko lapansi

Salmo la Asafu.

1Mulungu wa milungu, Yehova, wanena,
Aitana dziko lapansi kuyambira kuturuka kwa dzuwa kufikira kulowa kwace.
2Mulungu awalira m'Ziyoni, mokongola mwangwiro.
3Adzafika Mulungu wathu, ndipo sadzakhala cete:
Moto udzanyeka pankhope pace,
Ndipo pozungulira pace padzasokosera kwakukuru.
4Kumwamba adzaitana zakumwamba,
Ndi dziko lapansi, kuti aweruze anthu ace:
5Mundisonkhanitsire okondedwa anga;
Amene anapangana ndi Ine ndi nsembe.
6Ndipo zakumwamba zionetsera cilungamo cace;
Pakuti Mulungu mwini wace ndiye woweruza.
7Imvani, anthu anga, ndipo ndidzanena;
Israyeli, ndipo ndidzacita mboni pa iwe:
Ine Mulungu, ndine Mulungu wako.
8Sindikudzudzula iwe cifukwa ca nsembe zako;
Popeza nsembe zako zopsereza ziri pamaso panga cikhalire.
9Sindidzatenga ng'ombe m'nyumbamwako,
Kapena mbuzi m'makola mwako.
10Pakuti zamoyo zonse za kuthengo ndi zanga,
Ndi ng'ombe za pa mapiri zikwi.
11Ndidziwa mbalame zonse za m'mapiri:
Ndipo nyama za kuthengo ziri ndi Ine.
12Ndikamva njala, sindidzakuuza:
Pakuti dziko lonse ndi langa, ndi kudzala kwace komwe.
13Kodi ndidzadya nyama ya ng'ombe,
Kapena kumwa mwazi wa mbuzi?
14Pereka kwa Mulungu nsembe yaciyamiko;
Numcitire Wam'mwambamwamba cowinda cako:
15Ndipo undiitane tsiku la cisautso:
Ndidzakulanditsa, ndipo iwe udzandilemekeza.
16Koma kwa woipa Mulungu anena,
Uli nao ciani malemba anga kulalikira,
Ndi kuchula pangano langa pakamwa pako?
17Popeza udana naco cilangizo,
Nufulatira mau anga.
18Pakuona mbala, ubvomerezana nayo,
Nucita nao acigololo.
19Pakamwa pako mpocita zocimwa,
Ndipo lilime lako likonza cinyengo.

20Ukhala, nuneneza mbale wako;
Usinjirira mwana wa mai wako.
21Izi unazicita iwe, ndipo ndinakhala cete Ine;
Unayesa kuti ndifanana nawe:
Ndidzakudzudzula, ndi kucilongosola pamaso pako.
22Dziwitsani ici inu oiwala Mulungu,
Kuti ndingakumwetuleni, ndipo mungasowepo mpulumutsi:
23Wopereka nsembe yaciyamiko andilemekeza Ine;
Ndipo kwa iye wosunga mayendedwe ace
Ndidzamuonetsa cipulumutso ca Mulungu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 51

Davide abvomereza kucimwa kwace, apempha Mulungu amkhululukire, asamcotsere Mzimu Woyera

Kwa Mkulu wa Nyimbo. Salmo la Davide; m'mene anamdzera Natani mnenertso atalowa iye kwa Bateseba.

1Mundicitire ine cifundo, Mulungu,
Monga mwa kukoma mtima kwanu;
Monga mwa unyinji wa nsoni zokoma zanu
Mufafanize macimo anga.
2Mubwereze kunditsuka mphulupulu yanga,
Ndipo mundiyeretse kundicotsera coipa canga,
3Cifukwa ndazindikira macimo anga;
Ndipo coipa canga ciri pamaso panga cikhalire:
4Pa Inu, Inu nokha, ndinacimwa,
Ndipo ndinacicita coipaco pamaso panu:
Kuti mukhale wolungama pakulankhula Inu,
Mukhalenso woyera pa kuweruza kwanu.
5Onani, ndinabadwa m'mphulupulu:
Ndipo mai wanga anandilandira m'zoipa.
6Onani, Inu mukondwera ndi zoonadi m'malo a m'katimo;
Ndipo m'malo a m'tseri mudzandidziwitsa nzeru.
7Mundiyeretse ndi hisope ndipo ndidzayera;
Munditsuke ndipo ndidzakhala wa mbu woposa matalala.
8Mundimvetse cimwemwe ndi kusekera:
Kuti mafupawo munawatyola akondwere.
9Muzibisire nkhope yanu zolakwa zanga,
Ndipo mufafanize mphulupulu zanga zonse.
10Mundilengere mtima woyera, Mulungu;
Mukonze mzimu wokhazikika m'kati mwanga.
11Musanditaye kundicotsa pamaso panu;
Musandicotsere Mzimu wanu Woyera.
12Mundibwezere cimwemwe ca cipulumutso canu;
Ndipo mzimu wakulola undigwirizize.
13Pomwepo ndidzalangiza ocimwa njira zanu;
Ndipo olakwa adzabwera kwa Inu.
14Mundilanditse ku mlandu wa mwazi, Mulungu,
Ndinu Mulungu wa cipulumutso canga;
Lilime langalidzakweza Nyimbo ya cilungamo canu.
15Ambuye, tsegulani pa milomo yanga;
Ndipo pakamwa panga padzalalikira ulemekezo wanu.
16Pakuti simukondwera ndi nsembe, mwenzi nditapereka;
Nsembe yopsereza simuikonda.
17Nsembe za Mulungu ndizo mzimu wosweka;
Inu, Mulungu, simudzaupeputsa mtima wosweka ndi wolapa.

18Citirani Ziyoni cokoma monga mwa kukondwera kwanu;
Mumange malinga a miyala a Yerusalemu.
19Pamenepo mudzakondwera nazo nsembe zacilungamo,
Ndi nsembe yopsereza ndi yopsereza yathunthu:
Pamenepo adzapereka
Ng'ombe pa guwa lanu la nsembe.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 52

Davide aneneratu za cionongeko ca oipa, iye nakhulupirira Mulungu

Kwa Mkulu wa Nyimbo. Cilangizo ca Davide. Muja analowa Doegi M-edomu nauza Sauli, nati kwa iye, Davide walowa m'nyumba ya Abimeleke.

1Udzitamandiranji ndi coipa, ciphonaiwe?
Cifundo ca Mulungu cikhala tsiku lonse.
2Lilime lako likupanga zoipa;
Likunga lumo lakuthwa, lakucita monyenga.
3Ukonda coipa koposa cokoma;
Ndi bodza koposa kunena cilungamo.
4Ukonda mau onse akuononga, Lilime lacinyengo, iwe.
5Potero Mulungu adzakupasula ku nthawi zonse,
Adzakucotsa nadzakukwatula m'hema mwako,
Nadzakuzula, kukucotsa m'dziko la amoyo.
6Ndipo olungama adzaciona, nadzaopa,
Nadzamseka, ndi kuti,
7Tapenyani, suyu munthuyu amene sanamuyesa Mulungu mphamvu yace;
Amene anatama kucuruka kwa cuma cace,
Nadzilimbitsa m'kuipsa kwace.
8Koma ine ndine ngati mtengo wauwisi waazitona m'nyumba ya Mulungu:
Ndikhulupirira cifundo ca Mulungu ku nthawi za nthawi.
9Ndidzakuyamikani kosatha, popeza Inu munacicita ici:
Ndipo ndidzayembekeza dzina lanu, pakuti ici ncokoma, pamaso pa okondedwa anu,

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 53

Kupusa ndi kuipa kwa anthu

Kwa Mkulu wa Nyimbo; pa Mahalat. Cilanidzo ca Davide.

1Citsiru cimati mumtima mwace, Kulibe Mulungu.
Acita zobvunda, acita cosalungama conyansa;
Kulibe wakucita bwino.
2Mulungu m'mwamba anaweramira pa ana a anthu,
Kuti aone ngati aliko wanzeru, Wakufuna Mulungu.
3Onse anabwerera; anabvunda mtima pamodzi;
Palibe mmodzi wakucita bwino, nnena mmodzi.
4Kodi ocita zopanda pace sadziwa?
Pomadya anthu anga monga akudya mkate;
Ndipo saitana Mulungu.
5Pamenepo anaopa kwakukuru, popanda cifukwa ca kuopa:
Pakuti Mulungu anamwaza mafupa a iwo akuzinga iwe;
Unawacititsa manyazi, pakuti Mulungu anawakaniza.
6Ha, cipulumutso ca Israyeli cicokere m'Ziyoni!
Pakubweretsa Mulungu anthu ace a m'ndende,
Yakobo adzakondwera, Israyeli adzasekera.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 54

Davide apempha Mulungu amlanditse

Kwa Mkulu wa Nyimbo: pa Neginoto. Cilangizo ca Davide. Muja Azift anamuka nauza Sauli, kuti, Kodi Davide sabisala kwathu nanga?

1Ndipulumutseni, Mulungu, mwa dzina lanu,
Ndipo mundiweruze ndi mphamvuyanu.
2Imvani pemphero langa, Mulungu;
Cherani khutu mau a pakamwa panga.
3Pakuti alendo andiukira,
Ndipo oopsa afunafuna moyo wanga;
Sadziikira Mulungu pamaso pao.
4Taonani, Mulungu ndiye mthandizi wanga:
Ambuye ndiye wacirikiza moyo wanga.
5Adzabwezera coipa adani anga:
Aduleni m'coonadi canu.
6Ine mwini ndidzapereka nsembe kwa Inu:
Ndidzayamika dzina lanu, Yehova, pakuti nlokoma.
7Pakuti anandilanditsa m'nsautso yonse;
Ndipo ndapenya ndi diso langa ico ndakhumbira pa adani anga,

©The Bible Society of Malawi, 1992

Davide adandaula pa kuipa kwa adani, adziponya kwa Mulungu, nalangiza ena azitero iwo omwe

Kwa Mkulu wa Nyimbo: pa Zlrumbu. Cilanliizo ca Davide.

1Cherani khutu pemphero langa, Mulungu;
Ndipo musadzibisa pa kupemba kwanga.
2Mveram, ndipo mundiyankhe:
Ndiliralira m'kudandaula kwanga ndi kubuula;
3Cifukwa ca mau a mdani,
Cifukwa ca kundipsinja woipa;
Pakuti andisenza zopanda pace,
Ndipo adana nane mumkwiyo.
4Mtima wanga uwawa m'kati mwanga;
Ndipo zoopsa za imfa zandigwera.
5Mantha ndi kunjenjemera zandidzera,
Ndipo zoopsetsa zandikuta.
6Ndipo ndinati, Ha, wina akadandipatsa mapiko onga a njiwa
Mwenzi nditauluka, ndi kukhaliratu.
7Onani, ndikadathawira kutari,
Ndikadagona m'cipululu.
8Ndikadafulumira ndipulumuke
Ku mphepo yolimba ndi namondwe.
9Aonongeni, Ambuye, gawani lilime lao:
Pakuti ndaona ciwawa ndi ndeu m'mudzimo.
10Izizo ziuzungulira pa malinga ace usana ndi usiku;
Ndipo m'kati mwace muli zapanda pace ndi cobvuta.
11M'kati mwace muli kusakaza:
Ciwawa ndi cinyengo sizicoka m'makwalala ace.
12Pakuti si mdani amene ananditonzayo;
Pakadatero ndikadacilola:
Amene anadzikuza pa ine sindiye munthu wondida;
Pakadatero ndikadambisalira:
13Koma ameneyo ndiwe, munthu woyenerana nane,
Tsamwali wanga, wodziwana nane.
14Tinapangirana upo wokoma,
Tinaperekeza khamu la anthu popita ku nyumba ya Mulungu.
15Imfa iwagwere modzidzimutsa,
Atsikire kumanda ali amoyo:
Pakuti m'mokhala mwao muli zoipa pakati pao,
16Koma ine ndidzapfuulira kwa Mulungu;
Ndipo Yehova atizandipulumutsa.
17Madzulo, m'mawa, ndi msana ndidzadandaula, ndi kubuula,
Ndipo adzamva mau anga.

18Anaombola moyo wanga ku nkhondo yondilaka, ndikhale
mumtendere:
Pakuti ndiwo ambiri okangana nane.
19Mulungu adzamva, nadzawasautsa,
Ndiye wokhalabe ciyambire kale lomwe.
Popeza iwowa sasinthika konse,
Ndipo saopa Mulungu.
20Anaturutsa manja ace awagwire iwo akuyanjana naye:
Anaipsa pangano lace.
21Pakamwa pace mposalala ngati mafuta amkaka,
Koma mumtima mwace munali nkhondo:
Mau ace ngofewa ngati mafuta oyenga,
Koma anali malupanga osololasolola.
22Umsenze Yehova nkhawa zako, ndipo Iyeadzakugwiriziza:
Nthawi zonse sadzalola wolungama agwedezeke.
23Koma Inu, Mulungu, mudzawatsitsira ku dzenje la cionongeko:
Anthu okhetsa mwazi ndi acinyengo masiku ao sadzafikira nusu;
Koma ine ndidzakhulupirira Inu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 56

Davide apempha Mulungu amlanditse; ayamika atamlanditsa

Kwa Mkulu wa Nyimbo; pa Yonat-Elem Recokimu, Miktamu wa Davide, muja Afilisti anamgwira m'Gati.

1Mundicitire cifundo, Mulungu, pakuti anthu afuna kundimeza:
Andipsinja pondithira nkhondo tsiku lonse.
2Adani anga afuna kundimeza tsiku lonse:
Pakuti ambiri andithira nkhondo modzikuza.
3Tsiku lakuopa ine,
Ndidzakhulupirira Inu.
4Mwa Mulungu ndidzalemekeza mau ace:
Ndakhulupirira Mulungu, sindidzaopa;
Anthu adzandicitanji?
5Tsiku lonse atenderuza mau anga:
Zolingirira zao zonse ziri pa ine kundicitira coipa.
6Amemezana, alalira,
Achereza mapazi anga,
Popeza alindira moyo wanga.
7Kodi adzapulumuka ndi zopanda pace?
Gwetsani anthu mumkwiyo, Mulungu.
8Muwerenga kuthawathawa kwanga:
Sungani misozi yanga m'nsupa yanu;
Kodi siikhala m'buku mwanu?
9Pamenepo adani anga adzabwerera m'mbuyo tsiku lakuitana ine:
Ici ndidziwa, kuti Mulungu abvomerezana nane.
10Mwa Mulungu ndidzalemekeza mau ace:
Mwa Yehova ndidzalemekeza mau ace.
11Pa Mulungu ndakhulupirira, sindidzaopa;
Munthu adzandicitanji?
12Zowindira Inu Mulungu, ziri pa ine:
Ndidzakucitirani zoyamika.
13Pakuti mwalanditsa moyo wanga kuimfa:
Simunatero nao mapazi anga kuti ndingagwe?
Kuti ndiyende pamaso pa Mulungu
M'kuunika kwa amoyo.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 57

Davide apempha Mulungu amciniirize, namlemekezapo

Kwa Mkulu wa Nyimbo; pa Altasheti Miktamu wa Davide: muja anathawa Sauli au m'phanga.

1Mundicitire cifundo, Mulungu, mundicitire cifundo;
Pakuti moyo wanga ukhulupirira Inu:
Ndipo ndithawira ku mthunzi wa mapiko anu,
Kufikira zosakazazo zidzapita.
2Ndidzapfuulira kwa Mulungu Wam'mwambamwamba;
Ndiye Mulungu wonditsirizira zonse.
3Adzanditumizira m'mwamba, nadzandipulumutsa
Ponditonza wofuna kundimeza;
Mulungu adzatumiza cifundo cace ndi coonadi cace.
4Moyo wanga uli pakati pa mikango;
Ndigona pakati pa oyaka moto,
Ndiwo ana a anthu amene mano ao ali nthungo ndi mibvi,
Ndipo lilime lao ndilio lupanga lakuthwa.
5Mukwezeke m'mwambamwa mba, Mulungu;
Ulemerero wanu ukhale pamwamba pa dziko lonse lapansi.
6Anandichera ukonde apo ndiyenda;
Moyo wanga wawerama:
Anandikumbira mbuna patsogolo panga;
Anagwa m'kati mwace iwo okha.
7Mtima wanga wakhazikika, Mulungu, ndakhazika mtima;
Ndidzayimba, inde, ndidzayimba zolemekeza.
8Galamuka, ulemu wanga; galamukani cisakasa ndi zeze:
Ndidzauka ndekha mamawa.
9Ndidzakuyamikirani mwa anthu, Ambuye:
Ndidzakuyimbirani mwa mitundu.
10Pakuti cifundo canu ncacikuru kufikira m'mwamba,
Ndi coonadi canu kufikira mitambo.
11Kwezekani m'mwambamwamba, Mulungu;
Ulemerero wanu ukhale pamwamba m'dziko lonse lapansi.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 58

Davide adzudzula oipa Mulungu awalange

Kwa Mkulu wa Nyimbo; pa Altasyeti; Miktamu wa Davide.

1Kodi muli cete ndithu poyenera inu kunena zolungama?
Muweruza ana a anthu molunjika kodi?
2Inde, mumtima mucita zosalungama;
Pa dziko lapansi mugawira anthu ciwawa ca m'manja mwanu.
3Oipa acita cilendo cibadwire:
Asokera kuyambira kubadwa kwao, nanena bodza.
4Ululu wao ukunga wa njoka;
Akunga mphiri yogontha m'khutu, itseka m'khutu mwace.
5Imene simvera liu la oitana,
Akucita matsenga mocenieratu,
6Tyolani mano ao m'kamwa mwao, Mulungu:
Zulani zitsakano za misona ya mkango, Yehova.
7Apitetu ngati madzi oyenda;
Popiringidza mibvi yace ikhale yodukaduka.
8Apite ngati nkhono yosungunuka;
Asaone dzuwa monga mtayo,
9Miphika yanu isanagwire moto waminga,
Adzaiuluza, yaiwisi ndi yoyaka.
10Wolungama adzakondwera pakuona kubwezera cilango:
Adzasamba mapazi ace m'mwazi wa woipa.
11Ndipo anthu adzati, Indedi, pali mphotho kwa wolungama;
Indedi, pali Mulungu wakuweruza pa dziko lapansi.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 59

Davide apempha Mulungu amlanditse, nadzinenera wosalakwa

Kwa Mkulu wa Nyimbo; pa Altasbeti. Mikta mu wa Davide. Muja anatuma adikire nyumba yace, kuti amuphe,

1Ndilanditseni kwa adani anga, Mulungu wanga:
Ndiikeni pamsanje kwa iwo akundiukira.
2Mundilanditse kwa ocita zopanda pace,
Ndipo ndipulumutseni kwa anthu olira mwazi.
3Pakuti onani, alalira moyo wanga;
Amphamvu andipangira ciwembu:
Osacimwa, osalakwa ine, Yehova,
4Osawapatsa cifukwa ine, athamanga nadzikonza;
Galamukani kukomana nane, ndipo penyani.
5Ndinu Yehova, Mulungu wa makamu, Mulungu wa Israyeli,
Ukani kukazonda amitundu onse:
Musacitire cifundo mmodzi yense wakucita zopanda pace monyenga.
6Abwera madzulo, auwa ngati garu,
Nazungulira mudzi.
7Onani abwetuka pakamwa pao;
M'milomo mwao muli lupanga,
Pakuti amati, Amva ndani?
8Koma Inu, Yehova, mudzawaseka;
Mudzalalatira amitundu onse.
9Inu, mphamvu yanga, ndidzakulindirani;
Pakuti Mulungu ndiye msanje wanga.
10Mulungu wa cifundo canga adzandikumika:
Adzandionetsa tsoka la adani anga.
11Musawapheretu, angaiwale anthu anga:
Muwabalalitse mwa mphamvu yanu, ndipo muwagwetse,
Ambuye, ndinu cikopa cathu.
12Pakamwa pao acimwa ndi mau onse a pa milomo yao,
Potero akodwe m'kudzitamandira kwao,
Ndiponso cifukwa ca kutemberera ndi bodza azilankhula.
13Muwathe mumkwiyo, muwagurule psiti:
Ndipo adziwe kuti Mulungu ndiye woweruza m'Yakobo,
Kufikira malekezero a dziko la pansi.
14Ndipo abwere madzulo, auwe ngati garu,
Nazungulire mudzi.
15Ayendeyende ndi kufuna cakudya,
Nacezere osakhuta.
16Koma ine, ndidzayimbira mphamvu yanu;
Inde ndidzayimbitsa cifundo canu mamawa:
Pakuti Inu mwakhala msanje wanga,
Ndi pothawirapo ine tsiku la nsautso yanga.
17Ndidzayimbira zakukulemekezani Inu, mphamvu yanga:
Pakuti Mulungu ndiye msanje wanga, Mulungu wa cifundo canga.

Masalmo 60

Madandaulo ndi pempho la Davide

Kwa Mkulu wa Nyimbo pa Susan-Eduti. Miktamu wa Davide; lakulangiza: muja analimbana nao Aramnabaraimu ndi Aramzoba, nabwera Yoabu napha a Edomu m'Ciagwa ca Mcere zikwikhumi mpilambu Ziwiri.

1Mwatitaya Mulungu, mwatipasula;
Mwakwiya; tibwezereni.
2Mwagwedeza dziko, mwaling'amba:
Konzani ming'alu yace; pakuti ligwedezeka.
3Mwaonetsa anthu anu zowawa:
Mwatimwetsa vinyo wotinjenjemeretsa.
4Koma mwapatsa mbendera akuopa Inu,
Aikweze cifukwa ca coonadi.
5Kuti okondedwa anu alanditsidwe,
Pulumutsani ndi dzanja lanu lamanja, ndipo mutibvomereze.
6Mulungu walankhula m'ciyero cace; ndidzakondwerera:
Ndidzagawa Sekemu, ndidzayesa muyeso cigwa ca Sukoti.
7Gileadi ndi wanga, Manasenso ndi wanga;
Ndipo Efraimu ndi mphamvu ya mutu wanga;
Yuda ndiye wolamulira wanga,
8Moabu ndiye mkhate wanga;
Pa Edomu ndidzaponya nsapato yanga:
Filistiya, pfuulatu cifukwa ca ine.
9Adzandifikitsa ndani m'mudzi wa m'linga?
Adzanditsogolera ndani ku Edomu?
10Si ndinu, Mulungu, amene mwantaya?
Osaturuka nao makamu athu, Mulungu.
11Tithandizeni kunsautso;
Kuti cipulumutso ca munthu ndi cabe.
12Mwa Mulungu tidzacita molimbika mtima,
Ndipo Iye adzapondereza otisautsa.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 61

Poopsedwa Davide athamangira Mulungu

Kwa Mkulu wa Nyimbo; Neginoto. Salmo la Davide.

1Imvani mpfuu wanga, Mulungu;
Mverani pemphero langa.
2Ku malekezero a dziko lapansi ndidzapfuulira kwa Inu, pomizika mtima wanga:
Nditsogolereni ku thanthwe londiposa ine m'kutalika kwace.
3Pakuti munakhala pothawirapo panga; nsanja yolimba pathawa mdani ine.
4Ndidzagonera-gonerabe m'cihemamwanu;
Ndidzathawira mobisalamo m'mapiko anu.
5Pakuti Inu, Mulungu, mudamva zowinda zanga;
Munandipatsa colowa ca iwo akuopa dzina lanu.
6Mudzatalikitsa moyo wa mfumu:
Zaka zace zidzafikira mibadwo mibadwo.
7Adzakhala nthawi zonse pamaso pa Mulungu;
Mumpatse cifundo ndi coonadi zimsunge.
8Potero ndidzayimba zolemekeza dzina lanu ku nthawi zonse,
Kuti ndicite zowinda zanga tsiku ndi tsiku.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 62

Posautsidwa Davide athamangira Mulungu yekha

Kwa Mlrulu wa Nyimbo, pa Jedutunu. Salmo la Davide.

1Moyo wanga ukhalira cete Mulungu yekha:
Cipulumutso canga cifuma kwa Iye.
2Iye yekhayo ndiye thanthwe langa ndi cipulumutso canga;
Msanje wanga, sindidzagwedezeka kwakukuru.
3Mudzambvumbvulukira munthu mpaka liti,
Kumupha iye, nonsenu,
Monga khoma lopendekeka, ndi mpanda woweyeseka?
4Komatu amkhaliraupo kuti amkankhire pansi ulemu wace;
Akondwera nao mabodza;
Adalitsa ndi m'kamwa mwao, Koma atemberera mumtima.
5Moyo wanga, ukhalire cete Mulungu yekha;
Pakuti ciyembekezo canga cifuma kwa Iye,
6Iye yekhayo ndiye thanthwe langa ndi cipulumutso canga,
Msanje wanga, sindidzagwedezeka.
7Pa Mulungu pali cipulumutso canga ndi ulemerero wanga:
Thanthwe la mphamvu yanga ndi pothawirapo panga mpa Mulungu.
8Khulupirani pa Iye nyengo zonse, anthu inu:
Tsanulirani mitima yanu pamaso pace:
Mulungu ndiye pothawirapo ife.
9Indetu, anthu acabe ndi mpweya, ndipo anthu akuru ndi bodza:
Pakuwayesa apepuka;
Onse pamodzi apepuka koposa mpweya,
10Musakhulupirire kusautsa, ndipo musatama cifwamba;
Cikacuruka cuma musakhazikepo mitima yanu.
11Mulungu ananena kamodzi, ndinacimva kawiri:
Kuti mphamvu ndi yace ya Mulungu:
12Cifundonso ndi canu, Ambuye:
Cifukwa Inu musudzula munthu ali yense monga mwa nchito yace.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 63

Mtima woliralira kuyanfana ndi Mulungu

Salmo la Davide; muja akakhala m'cipululu ca Yuda.

1Inu Mulungu, ndinu Mulungu wanga; ndidzakufunani m'matanda kuca:
Moyo wanga ukumva ludzu la kwa Inu, thupi langa lilirira Inu,
M'dziko louma ndi lotopetsa, lopanda madzi.
2Kuti ndione mphamvu yanu ndi ulemerero wanu,
Monga ndinakuonani m'malo oyera.
3Pakuti cifundo canu ciposa moyo makomedwe ace;
Milomo yanga idzakulemekezani.
4Potero ndidzakuyamikani m'moyo mwanga;
Ndidzakweza manja anga m'dzina lanu.
5Mudzakhutitsa moyo wanga ngati ndi mafuta ndi zonona;
Ndipo pakamwa panga ndidzakulemekezani ndi milomo yakupfuula mokondwera;
6Pokumbukira Inu pa kama wanga,
Ndi kulingalira za Inu maulonda a usiku.
7Pakuti munakhala mthandizi wanga;
Ndipo ndidzapfuula mokondwera mu mthunzi wa mapiko anu.
8Moyo wanga uumirira Inu:
Dzanja lamanja lanu lindigwiriziza.
9Koma iwo amene afuna moyo wanga kuti auononge,
Adzalowa m'munsi mwace mwa dziko.
10Adzawapereka ku mphamvu ya lupanga;
Iwo adzakhala gawo la ankhandwe.
11Koma mfumu idzakondwera mwa Mulungu;
Yense wakulumbirira iye adzatamandira;
Pakuti pakamwa pa iwo onena bodza padzatsekedwa.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 64

Davide apempha Mulungu amciniirize pa omlalira

Kwa Mkulu wa Nyimbo. Salmo la Davido.

1Imvani Yehova, mau anga, m'kudandaula kwanga;
Sungani moyo wanga angandiopse mdani.
2Ndibiseni pa upo wacinsinsi wa ocita zoipa;
Pa phokoso la ocita zopanda pace:
3Amene anola lilime lao ngati lupanga,
Napiringidza mibvi yao, ndiyo mau akuwawitsa;
4Kuponyera wangwiro mobisika:
Amponyera modzidzimutsa, osaopa.
5Alimbikitsana m'cinthu coipa;
Apangana za kuchera misampha mobisika;
Akuti, Adzaiona ndani?
6Afunafuna zosalungama; kusanthula, asanthuladi kutha;
Cingakhale ca m'kati mwace mwa munthu, ndi mtima wozama.
7Koma Mulungu adzawaponyera mubvi;
Adzalaswa modzidzimutsa,
8Adzawakhumudwitsa, lilime lao lidzawatsutsa;
Onse akuwaona adzawathawa.
9Ndipo anthu onse adzacita mantha;
Nadzabukitsa cocita Mulungu,
Nadzasamalira nchito yace.
10Wolungama adzakondwera mwa Yehova, nadzakhulupirira Iye;
Ndipo oongoka mtima onse adzalemekeza.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 65

Davide alemekeza Mulungu pa madalitso ocuruka

Kwa Mkulu wa Nyimbo; Salimo, nyimbo ya Davide.

1M'Ziyoni akulemekezani Inu mwacete, Mulungu:
Adzakucitirani Inu cowindaci.
2Wakumva pemphero Inu,
Zamoyo zonse zidzadza kwa Inu.
3Mphulupulu zinandilaka;
Koma mudzafafaniza zolakwa zathu.
4Wodala munthuyo mumsankha, ndi kumyandikizitsa,
Akhale m'mabwalo anu:
Tidzakhuta nazo zokoma za m'nyumba yanu,
Za m'malo oyera a Kacisi wanu.
5Mudzatiyankha nazo zoopsa m'cilungamo,
Mulungu wa cipulumutso cathu;
Ndinu cikhulupiriko ca malekezero Onse a dziko lapansi,
Ndi ca iwo okhala kutali kunyanja:
6Ndinu amene mukhazikitsa mapiri ndi mphamvu yanu;
Pozingidwa naco cilimbiko.
7Amene atontholetsa kukuntha kwa nyanja, kukuntha kwa mafunde ace,
Ndi phokoso la mitundu ya anthu.
8Ndipo iwo akukhala kumalekezero adzacita mantha cifukwa ca zizindikilo zanu; Mukondweretsa apo paturukira dzuwa, ndi apo lilowera.
9Muceza nalo dziko lapansi, muhthirira,
Mulilemeza kwambiri;
Mtsinje wa Mulungu udzala nao madzi:
Muwameretsera tirigu m'mene munakonzera nthaka.
10Mukhutitsa nthaka yace yolima;
Mufafaniza nthumbira zace?
Muiolowetsa ndi mbvumbi;
Mudalitsa mmera wace.
11Mubveka cakaci ndi ukoma wanu;
Ndipo mabande anu akukha zakuca.
12Akukha pa mabusa a m'cipululu;
Ndipo mapiri azingika naco cimwemwe.
13Podyetsa mpodzaza ndi zoweta;
Ndipo zigwa zakutidwa ndi tirigu;
Zipfuula mokondwera, inde ziyimbira.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 66

Acenjeza onse alemekeze Mulungu pa nchito zace zodabwiza

Kwa Mkulu wa Nyimbo. Nyimbo. Salmo.

1Pfuulirani kwa Mulungu, dziko lonse lapansi.
2Yimbirani ulemerero wa dzina lace;
Pomlemekeza mumcitire ulemerero.
3Nenani kwa Mulungu, Ha, nchito zanu nzoopsa nanga!
Cifukwa ca mphamvu yanu yaikuru adani anu adzagonjera Inu,
4Dziko lonse lapansi lidzakugwadirani,
Ndipo lidzakuyimbirani;
Adzayimbira dzina lanu.
5Idzani, muone nchito za Mulungu;
Zocitira Iye ana a anthu nzoopsa.
6Anasanduliza nyanja ikhale mtunda:
Anaoloka mtsinje coponda pansi:
Apo tinakondwera mwa Iye.
7Acita ufumu mwa mphamvu yace kosatha;
Maso ace ayang'anira amitundu;
Opikisana ndi Iye asadzikuze.
8Lemekezani Mulungu wathu, mitundu ya anthu inu,
Ndipo mumveketse liu la cilemekezo cace:
9Iye amene asunga moyo wathu tingafe,
Osalola phazi lathu literereke.
10Pakati munatiyesera, Mulungu:
Munatiyenga monga ayenga siliya.
11Munapita nafe kuukonde;
Munatisenza cothodwetsa pamsana pathu.
12Munapititsa anthu oberekeka pamwamba pamitu pathu;
Tinapyola moto ndi madzi; Koma munatifikitsa potitsitsimutsa.
13Ndidzalowa m'nyumba yanu ndi nsembe zopsereza,
Ndidzakucitirani zowinda zanga,
14Zimene inazichula milomo yanga,
Ndinazinena pakamwa panga pasautsika ine.
15Ndidzakufukizirani nsembe zapsereza zonona,
Pamodzi ndi cofukiza ca mphongo za nkhosa;
Ndidzakonza ng'ombe pamodzi ndi mbuzi.
16Idzani, imvani, inu nonse akuopa Mulungu,
Ndipo ndidzafotokozera zonse anazicitira moyo wanga,
17Ndinampfuulira Iye pakamwa panga,
Ndipo ndinamkuza ndi lilime langa,
18Ndikadasekera zopanda pace m'mtima mwanga,
Ambuye sakadamvera:
19Koma Mulungu anamvadi; Anamvera mau a pemphero langa,
20Wolemekezeka Mulungu,

Amene sanandipatutsira ine pemphero langa, kapena cifundo cace.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 67

Amitundu alemekeze Mulungu

Kwa Mkulu wa Nyimbo, pa Neginolo. Salmo, Nyimbo.

1Aticitire cifundo Mulungu, ndi kutidalitsa,
Atiwalitsire nkhope yace;
2Kuti njira yanu idziwike pa dziko lapansi,
Cipulumutso canu mwa amitundu onse.
3Anthu akuyamikeni, Mulungu;
Anthu onse akuyamikeni.
4Anthu akondwere, napfuule makondwera;
Pakuti mudzaweruza anthu malunjika,
Ndipo mudzalangiza anthu pa dziko lapansi.
5Anthu akuyamikeni, Mulungu;
Anthu onse akuyamikeni.
6Dziko lapansi lapereka zipatso zace:
Mulungu, Mulungu wathu adzatidalitsa.
7Mulungu adzatidalitsa;
Ndipo malekezero onse a dziko lapansi adzamuopa Iye,

©The Bible Society of Malawi, 1992

Mau akuyamikira Mulungu wa cipulumutso conse
Kwa Mkulu wa Nyimbo. Salmo la Davide. Nyimbo

1Auke Mulungu, abalalike adani ace;
Iwonso akumuda athawe pamaso pace.
2Muwacotse monga utsi ucotseka; Monga phula lisungunuka pamoto,
Aonongeke oipa pamaso pa Mulungu.
3Koma olungama akondwere; atumphe ndi cimwemwe pamaso pa Mulungu;
Ndipo asekere naco cikondwerero.
4Yimbirani Yehova, liyimbireni Nyimbo dzina lace;
Undirani mseu Iye woberekekayo kucidikha;
Dzina lace ndiye Yehova; ndipo tumphani ndi cimwemwe pamaso pace.
5Mulungu, mokhala mwace mayera,
Ndiye Atate wa ana amasiye, ndi woweruza wa akazi amasiye.
6Mulungu amangitsira banjaanthu a pa okha;
Aturutsa am'ndende alemerere;
Koma opikisana naye akhala m'dziko lopanda madzi.
7Pakuturuka paja, Inu Mulungu, ndi kutsogolera anthu anu,
Pakuyenda paja Inu m'cipululu;
8Dziko lapansi linagwedezeka,
Inde thambo linakhapamaso pa Mulungu;
Sinai lomwe linagwedezeka pamaso pa Mulungu, Mulungu wa Israyeli.
9Inu, Mulungu, munabvumbitsa cimvula,
Munatsitsimutsa colowa canu pamene cidathodwa.
10Gulu lanu linakhala m'dziko muja:
Mwa ukoma wanu munalikonzera ozunzika, Mulungu.
11Ambuye anapatsa mau:
Akazi akulalikira uthengawo ndiwo khamu lalikuru.
12Mafumu a magulu a ankhondo athawathawa:
Ndipo mkazi amene akhala kwao agawa zofunkha.
13Pogona inu m'makola a zoweta,
Mukhala ngati mapiko a njiwa okulira ndi siliva,
Ndi nthenga zace zokulira ndi golidi woyenga wonyezimira.
14Pamene Wamphamvuyonse anabalalitsa mafumu m'dzikomo,
Munayera ngati matalala m'Salimoni.
15Phiri la Basana ndilo phiri la Mulungu;
Phiri la Basana ndilo phiri la mitu mitu.
16Mucitiranji nsanje mapiri inu a mitu mitu,
Ndi phirilo Mulungu analikhumba, akhaleko?
Inde, Yehova adzakhalabe komweko kosatha.

17Magareta a Mulungu ndiwo zikwi makumi awiri, inde zikwi zowirikiza-wirikiza:
Ambuye ali pakati pao, monga m'Sinai, m'malo opatulika,
18Munakwera kumka kumwamba, munapita nao undende kuuyesa ndende;
Munalandira zaufulu mwa anthu,
Ngakhale mwa opikisana nanu, kuti Yehova Mulungu akakhale nao.
19Wolemekezeka Ambuye, tsiku ndi tsiku atisenzera katundu,
Ndiye Mulungu wa cipulumutso cathu.
20Mulungu akhala kwa ife Mulungu wa cipulumutso;
Ndipo Yehova Ambuye ali nazo zopulumutsira kuimfa.
21Indedi Mulungu adzaphwanya mutu wa adani ace,
Pakati pa mutu pa iye woyendabe m'kutsutsika kwace.
22Ambuye anati, Ndidzawatenganso ku Basana,
Ndidzawatenganso kozama kwa nyanja:
23Kuti ubviike phazi lako m'mwazi,
Kuti malilime a agaru ako alaweko adani ako.
24Anapenya mayendedwe anu, Mulungu,
Mayendedwe a Mulungu wanga, Mfumu yanga, m'malo oyera.
25Oyimbira anatsogolera, oyimba zoyimba anatsata m'mbuyo,
Pakatipo anamwali oyimba mangaka.
26Lemekezani Mulungu m'masonkhano,
Ndiye Ambuye, inu a gwero la Israyeli.
27Apo pali Benjamini wamng'ono, wakuwacita ufumu,
Akuru a Yuda, ndi a upo wao,
Akulu a Zebuloni, akulu a Naftali.
28Mulungu wako analamulira mphamvu yako:
Limbitsani, Mulungu, cimene munaticitira.
29Cifukwa ca Kacisi wanu wa m'Yerusalemu
Mafumu adzabwera naco caufulu kukupatsani.
30Dzudzulani cirombo ca m'bango,
Khamu la mphongo ndi zipfululu za anthu,
Yense wakudzigonjera ndi ndarama zasiliva;
Anabalalitsa mitundu ya anthu ya kukondwera nayo nkhondo.
31Akulu adzafumira ku Aigupto;
Kushi adzafulumira kutambalitsa manja ace kwa Mulungu.
32Yimbirani Mulungu, maufumu a dziko lapansi inu;
Yimbirani Ambuye zomlemekeza;
33Kwa Iye wakuberekeka pamwambamwamba, oyambira kale lomwe;
Taonani; amveketsa liu lace, ndilo liu lamphamvu.
34Bvomerezani kuti mphamvu nja Mulungu;
Ukulu wace uli pa Israyeli,
Ndi mphamvu yace m'mitambo.

35Inu Mulungu, ndinu woopsa m'malo oyera anu;
Mulungu wa Israyeli ndiye amene apatsa anthu ace mphamvu ndi cilimbiko.
Alemekezeke Mulungu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 69

Davide adandaulira kwa Mulungu cifukwa ca zowawa azimva

Kwa Mkulu wa Nyimbo. Pa Syosyanimu. Salmo la Davide.

1Ndipulumutseni Mulungu;
Pakuti madzi afikira moyo wanga.
2Ndamira m'thope lozama, lopanda poponderapo;
Ndalowa m'madzi ozama, ndipo cigumula candimiza.
3Ndalema ndi kupfuula kwanga; kum'mero kwauma gwa:
M'maso mwanga mwada poyembekeza Mulungu wanga.
4Ondida kopanda cifukwa acuruka koposa tsitsi la pamutu panga;
Ofuna kunditha, ndiwo adani anga monama, ali ndi mphamvu:
Pamenepo andibwezetsa cosafunkha ine.
5Mulungu, mudziwa kupusa kwanga;
Ndipo kutsutsika kwanga sikubisikira Inu.
6Iwo akuyembekeza Inu, Ambuve Yehova wa makamu, asacite manyazi cifukwa ca ine:
Iwo ofuna Inu, Mulungu wa Israyeli, asapepulidwe cifukwa ca ine.
7Pakuti ndalola cotonza cifukwa ca Inu:
Cimpepulo cakuta nkhope yanga,
8Abale anga andiyesa mlendo,
Ndi ana a mai wanga andiyesa wa mtundu wina.
9Pakuti cangu ca pa nyumba yanu candidya;
Ndi zotonza za iwo otonza Inu zandigwera ine.
10Ndipo ndinalira pa kusala kwa moyo wanga,
Koma uku kunandikhalira cotonza.
11Ndipo cobvala canga ndinayesa ciguduli,
Koma amandiphera mwambi.
12Okhala pacipata akamba za ine; Ndipo oledzera andiyimba.
13Koma ine, pemphero langa liri kwa Inu, Yehova, m'nyengo yolandirika;
Mulungu, mwa cifundo canu cacikuru,
Mundibvomereze ndi coonadi ca cipulumutso canu.
14Mundilanditse kuthope, ndisamiremo:
Ndilanditseni kwa iwo akundida, ndi kwa madzi ozama.
15Cigumula cisandifotsere,
Ndipo cakuya cisandimize;
Ndipo asanditsekere pakamwa pace pa dzenje.
16Mundiyankhe Yehova; pakuti cifundo canu ncokoma;
Munditembenukire monga mwa unyinji wa nsoni zokoma zanu.
17Ndipo musabisire nkhope yanu mtumiki wanu;
Pakuti ndisautsika ine; mundiyankhe msanga.
18Yandikizani moyo wanga, ndi kuuombola;
Ndipulumutseni cifukwa ca adani anga,
19Mudziwa cotonza canga, ndi manyazi anga, ndi cimpepulo canga:

Akundisautsa ali pamaso panu,
20Cotonza candiswera mtima, ndipo ndidwala ine;
Ndipo ndinayembekeza wina wondicitira cifundo, koma palibe;
Ndinayembekeza onditonthoza mtima, osawapeza.
21Ndipo anandipatsa ndulu ikhale cakudya canga;
Nandimwetsa vinyo wosasa pomva ludzu ine.
22Gome lao likhale msampha pamaso pao;
Pokhala ndi mtendere iwo, likhale khwekhwe.
23M'maso mwao mude, kuti asapenye;
Ndipo munjenjemeretse m'cuuno mwao kosalekeza.
24Muwatsanulire mkwiyo wanu, Ndipo moto wa ukali wanu uwagwere.
25Pokhala pao pakhale bwinja;
M'mahema mwao musakhale munthu.
26Pakuti alondola amene Inu munampanda;
Ndipo akambirana za zowawa zao za iwo amene munawalasa.
27Onjezani mphulupulu pa mphulupulu zao;
Ndipo asafikire cilungamo canu.
28Afafanizidwe m'buku lamoyo,
Ndipo asalembedwe pamodzi ndi olungama,
29Koma ine ndine wozunzika ndi womva zowawa;
Cipulumutso canu, Mulungu, cindikweze pamsanje.
30Ndidzalemekeza dzina la Mulungu ndi kuliyimbira,
Ndipo ndidzambukitsa ndi kumyamika.
31Ndipo cidzakomera Yehova koposa ng'ombe,
Inde mphongo za nyanga ndi ziboda,
32Ofatsa anaciona, nakondwera:
Ndipo inu, ofuna Mulungu, mtima wanu ukhale ndi moyo.
33Pakuti Yehova amvera aumphawi,
Ndipo sapeputsa am'ndende ace.
34Zakumwamba ndi dziko lapansi zimlemekeze,
Nyanja ndi zonse zoyenda m'mwemo;
35Pakuti Mulungu adzapulumutsa Ziyoni, nadzamanga midzi ya Yuda;
Ndipo iwo adzakhala komweko, likhale lao lao.
36Ndipo mbumba ya atumiki ace idzalilandira;
Ndipo iwo akukonda dzina lace adzakhalam'mwemo.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 70

Davide apempha Mulungu amlanditse msanga

Kwa Mkulu wa Nyimbo: cikumbutso ca Davtde,

1Fulumirani kundipulumutsa, Mulungu;
Fulumirani kundithandiza, Yehova.
2Acite manyazi, nadodome
Amene afuna moyo wanga:
Abwezedwe m'mbuyo, napepulidwe.
Amene akonda kundicitira coipa,
3Abwerere, kukhale mphotho ya manyazi ao
Amene akuti, Hede, hede.
4Asekerere nakondwerere mwa Inu onse akufuna Inu;
Nanene kosalekeza iwo akukonda cipulumutso canu,
Abuke Mulungu.
5Koma ine ndine wozunzika ndi waumphawi;
Mundifulumirire, Mulungu:
Inu ndinu mthandizi wanga ndi mpulumutsi wanga;
Musacedwe, Yehova.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 71

Nkhalamba idziponya kwa Mulungu amene anamkhulupira kuyambira ubwana wace

1Ndikhulupirira Inu, Yehova:
Ndisacite manyazi nthawi zonse.
2Ndikwatuleni m'cilungamo canu, ndi kundilanditsa:
Ndicherereni khutu lanu ndi kundipulumutsa.
3Mundikhalire thanthwe lokhalamo, lopitako kosaleka;
Mwalamulira kundipulumutsa;
Popeza Inu ndinu thanthwe langa ndi linga langa,
4Ndilanditseni, Mulungu wanga, m'dzanja la woipa,
M'dzanja la munthu wosalungama ndi waciwawa.
5Pakuti Inu ndinu ciyembekezo canga, Ambuye Yehova;
Mwandikhalira wokhulupirika kuyambira ubwana wanga.
6Inu munandigwirizizakuyambira ndisanabadwe:
Kuyambira pa thupi la mai wanga wondicitira zokoma ndinu;
Ndidzakulemekezani kosalekeza.
7Ndikhala codabwiza kwa ambiri;
Koma Inu ndinu pothawira panga polimba.
8M'kamwa mwanga mudzadzala lemekezo lanu,
Ndi ulemu wanu tsiku lonse.
9Musanditaye mu ukalamba wanga;
Musandisiye, pakutha mphamvu yanga.
10Pakuti adani anga alankhula za ine;
Ndipo iwo akulalira moyo wanga apangana upo,
11Ndi kuti, Wamsiya Mulungu:
Mlondoleni, mgwireni; popeza palibe wompulumutsa,
12Musandikhalire kutali, Mulungu;
Fulumirani kundithandiza, Mulungu;
13Adani a moyo wanga acite manyazi, nathawe;
Cotonza ndi cimpepulo zikute ondifunira coipa,
14Koma ine ndidzayembekeza kosaleka,
Ndipo ndidzaonjeza kukulemekezani.
15Pakamwa panga padzafotokozera cilungamo canu,
Ndi cipulumutso canu tsiku lonse;
Pakuti sindidziwa mawerengedwe ace.
16Ndidzamuka mu mphamvu ya Ambuye Yehova;
Ndidzachula cilungamo canu, inde canu cokha.
17Mulungu, mwandiphunzitsa kuyambira ubwana wanga;
Ndipo kufikira lero ndilalikira zodabwiza zanu.
18Poteronso pokalamba ine ndi kukhala nazo imvi musandisiye,
Mulungu;
Kufikira nditalalikira mbadwo uwu za dzanja lanu,
Mphamvu yanu kwa onse akudza m'mbuyo.

19Cilungamo canunso, Mulungu, cifikira kuthambo;
Inu amene munacita zazikuru,
Akunga Inu ndani, Mulungu?
20Inu, amene munationetsa nsautso zambiri ndi zoipa,
Mudzatipatsanso moyo,
Ndi kutitenganso munsi mwa dziko.
21Mundionjezere ukulu wanga,
Ndipo munditembenukire kundisangalatsa,
22Ndiponso ndidzakuyamikani ndi cisakasa,
Kubukitsa coonadi canu, Mulungu wanga;
Ndidzakuyimbirani Nyimbo ndi zeze,
Ndinu Woyerayo wa Israyeli.
23Milomo yanga idzapfuula mokondwera poyimbira Inu Nyimbo;
Inde, moyo wanga umene munaombola.
24Lilime langa lomwe lidzalankhula za cilungamo canu tsiku lonse:
Pakuti ofuna kundicitira coipa acita manyazi, nadodoma.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Za ufumu wa Mfumu yokoma

Salimo la kwa Solomo.

1Patsani mfumu maweruzo anu, Mulungu,
Ndi mwana wa mfumu cilungamo canu.
2Potero adzanenera anthu anu mlandu ndi m'cilungamo,
Ndi ozunzika anu ndi m'ciweruzo.
3Mapiri adzatengera anthu mtendere,
Timapiri tomwe, m'cilungamo.
4Adzaweruza ozunzika a mwa anthu,
Adzapulumutsa ana aumphawi,
Nadzaphwanya wosautsa.
5Adzakuopani momwe likhalira dzuwa ndi mwezi,
Kufikira mibadwo mibadwo.
6Adzanga mvula yakugwa pa udzu wosenga:
Monga mvula yothirira dziko.
7Masiku ace wolungama adzakhazikika;
Ndi mtendere wocuruka, kufikira sipadzakhala mwezi.
8Ndipo adzacita ufumu kucokera kunyanja kufikira kunyanja,
Ndi kucokera ku Mtsinje kufikira malekezero a dziko lapansi.
9Okhala m'cipululu adzagwadira pamaso pace;
Ndi adani ace adzaluma nthaka.
10Mafumu a ku Tarisi ndi ku Zisumbuzo adzabwera naco copereka;
Mafumu a ku Sheba ndi Seba adzadza nazo mphatso,
11Inde mafumu onse adzamgwadira iye:
Amitundu onse adzamtumikira.
12Pakuti adzapulumutsa waumphawi wopfuulayo;
Ndi wozunzika amene alibe mthandizi.
13Adzacitira nsoni wosauka ndi waumphawi,
Nadzapulumutsa moyo wa aumphawi,
14Adzaombola moyo wao ku cinyengo ndi ciwawa;
Ndipo mwazi wao udzakhala wa mtengo pamaso pace:
15Ndipo iye adzakhala ndi moyo; ndipo adzampatsa golidi wa ku Sheba;
Nadzampempherera kosalekeza;
Adzamlemekeza tsiku lonse.
16M'dzikomo mudzakhala dzinthu dzocuruka pamwamba pa mapiri;
Zipatso zace zidzati waa, ngati za ku Lebano:
Ndipo iwo a m'mudzi adzaphuka ngati msipu wapansi.
17Dzina lace lidzakhala kosatha:
Momwe likhalira dzuwa dzina lace lidzamvekera zidzukulu:
Ndipo anthu adzadalitsidwa mwa Iye;
Amitundu onse adzamucha wodala.
18Wolemekezeka Yehova Mulungu, Mulungu wa Israyeli,

Amene acita zodabwiza yekhayo:
19Ndipo dzina lace la ulemerero lidalitsike kosatha;
Ndipo dziko lonse lapansi lidzale nao ulemerero wace.
Amen, ndi Amen.
20*Mapemphero a Davide mwana wa Jese atha.*

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 73

Kupindula kwa oipa kumakayikitsa pa cilungamo ca Mulungu, koma citsiriziro cao citibvomerezetsa cilungamoco

Salimo la Asafu.

1Indedi Mulungu acitira Israyeli zabwino,
Iwo a mtima wa mbe.
2Koma ine, ndikadagwa; Mapazi anga akadaterereka,
3Pakuti ndinacitira nsanje odzitamandira,
Pakuona mtendere wa oipa,
4Pakuti palibe zomangira pakufa iwo:
Ndi mphamvu yao niolimba,
5Sabvutika monga anthu ena;
Sasautsika monga anthu ena.
6Cifukwa cace kudzikuza kunga unyolo pakhosi pao;
Acibvala ciwawa ngati malaya.
7Kunenepa kwao kutuzulitsa maso ao:
Malingaliro a mitima yao asefukira.
8Acita zaphwete nalankhula moipa za kusautsa:
Alankhula modzitama.
9Pakamwa pao anena zam'mwamba,
Ndipo lilime lao liyendayenda m'dziko lapansi.
10Cifukwa cace anthu ace amabwera kudza kuno:
Ndipo cikho codzala ndi madzi acigugudiza.
11Namati, Akacidziwa bwanji Mulungu?
Kodi Wam'mwambamwamba ali nayonzeru?
12Tapenyani, oipa ndi awa;
Ndipo pokhazikika cikhazikikire aonjezerapo pa cuma cao.
13Indedi, ndinayeretsa mtima wanga kwacabe,
Ndipo ndinasamba m'manja mosalakwa;
14Popeza andisautsa tsiku lonse,
Nandilanga mamawa monse,
15Ndikadati, Ndidzafotokozera cotere,
Taonani, ndikadacita cosakhulupirika ndi mbadwo wa ana ako.
16Pamene ndinayesa kudziwitsa ici,
Ndinabvutika naco;
17Mpaka ndinalowa m'zoyera za Mulungu,
Ndi kulingalira citsiriziro cao.
18Indedi muwaika poterera:
Muwagwetsa kuti muwaononge.
19Ha! m'kamphindi ayesedwa bwinja;
Athedwa konse ndi zoopsya.
20Monga anthu atauka, apepula loto;
Momwemo, Inu Ambuye, pakuuka mudzapeputsa cithunzithunzi cao.

21Pakuti mtima wanga udawawa,
Ndipo ndinalaswa m'imso zanga;
22Ndinali wam'thengo, wosadziwa kanthu;
Ndinali ngati nyama pamaso panu.
23Koma ndikhala ndi Inu cikhalire:
Mwandigwira dzanja langa la manja.
24Mudzanditsogolera ndi uphungu wanu,
Ndipo mutatero, mudzandilandira m'ulemerero,
25Ndiri ndi yani Kumwamba, koma Inu?
Ndipo Pa dziko lapansi palibe wina wondikonda koma Inu.
26Likatha thupi langa ndi mtima wanga:
Mulungu ndiye thanthwe la mtima wanga, ndi colandira canga cosatha.
27Pakuti, taonani, iwo okhala patali ndi Inu adzaonongeka;
Muononga onse akupembedza kwina, kosiyana ndi Inu.
28Koma ine, kundikomera kuyandikiza kwa Mulungu:
Ndimuyesa Ambuye Yehova pathawirapo ine,
Kuti ndifotokozere nchito zanu zonse,

©The Bible Society of Malawi, 1992

Malo oyera adetsedwa. Apempha Mulungu akumbuke cipangano cao

Cilangizo ca Asaru.

1Mulungu, munatitayiranji citayire?
Mkwiyo wanu ufukiranji pa nkhosa za kubusa kwanu?
2Kumbukilani msonkhano wanu, umene munaugula kale,
Umene munauombola ukhale pfuko la colandira canu;
Phiri La Ziyoni limene mukhalamo.
3Nyamulani mapazi anu kukapenya mapasukidwe osatha,
Zoipa zonse adazicita mdani m'malo opatulika.
4Otsutsana ndi Inu abangula pakati pa msonkhano wanu;
Aika mbendera zao zikhale zizindikilo.
5Anaoneka ngati osamula nkhwangwa kunkhalango.
6Ndipo tsopano aphwanya zosemeka zace zonse
Ndi nkhwangwa ndi nyundo,
7Anatentha malo anu opatulika;
Anaipsa ndi kugwetsa pansi mokhalamo dzina lanu.
8Ananena mumtima mwao, Tiwapasule pamodzi;
Anatentha zosonkhaniramo za Mulungu zonse, m'dzikomo.
9Sitiziona zizindikilo zathu;
Palibenso mneneri;
Ndipo mwa ife palibe wina wakudziwa mpaka liti.
10Wotsutsanayo adzatonza kufikira liti, Mulungu?
Kodi mdani adzanyoza dzina lanu nthawi yonse?
11Mubwezeranji dzanja lanu, ndilo dzanja lamanja lanu?
Muliturutse ku cifuwa canu ndipo muwatheretu.
12Koma Mulungu ndiye mfumu yanga kuyambira kale,
Wocita zakupulumutsa pakati pa dziko lapansi.
13Mudagawa nyanja ndi mphamvu yanu;
Mudaswa mitu ya zoopsa za m'madzi.
14Mudaphwanya mitu ya livyatanu;
Mudampereka akhale cakudya ca iwo a m'cipululu.
15Mudagawa kasupe ndi mtsinje;
Mudaphwetsa mitsinje yaikuru.
16Usana ndi wanu, usikunso ndi wanu:
Munakonza kuunika ndi dzuwa.
17Munaika malekezero onse a dziko lapansi;
Munalenga dzinja ndi malimwe.
18Mukumbukile ici, Yehova, mdaniyo anatonza,
Ndipo anthu opusa ananyoza dzina lanu.
19Musapereke moyo wa njiwa yanu kwa cirombo;
Musamaiwala moyo wa ozunzika anu nthawi yonse.
20Samalirani cipanganoco;

Pakuti malo amdima a m'dziko adzala ndi zokhalamo ciwawa.
21Okhalira mphanthi asabwere nao manyazi;
Wozunzika ndi waumphawi alemekeze dzina lanu.
22Nyamukani, Mulungu, mudzinenere mlandu nokha;
Kumbukilani momwe akutonzani wopusa tsiku lonse.
23Musaiwale mau a iwo otsutsana ndi Inu;
Kusokosera kwa iwo akuukirani Inu kumakweca kosaleka.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 75

Mulungu woweruza asiyanitsa pakati pa odzikuza ndi olungama

Kwa Mkulu wa Nyimbo: Altasayeti: Salmo la Asafu. Nyimbo.

1Tikuyamikani Inu, Mulungu; Tiyamika, pakuti dzina lanu liri pafupi;
Afotokozera zodabwiza zanu,
2Pakuona nyengo yace ndidzaweruza molunjika.
3Lasungunuka dziko lapansi, ndi onse okhalamo;
Ndinacirika mizati yace.
4Ndinati kwa odzitamandira, Musamacita zodzitamandira;
Ndi kwa oipa, Musamakweza nyanga;
5Musamakwezetsa nyanga yanu;
Musamalankhula ndi khosi louma.
6Pakuti kukuzaku sikucokera kum'mawa,
Kapena kumadzulo, kapena kucipululu,
7Pakuti Mulungu ndiye woweruza;
Acepsa wina, nakuza wina.
8Pakuti m'dzanja la Yehova muli cikho;
Ndi vinyo wace acita thobvu;
Cidzala ndi zosanganizira, ndipo atsanulako:
Indedi, oipa onse a pa dziko lapansi adzamwa
Nadzagugudiza nsenga zace.
9Koma ine ndidzalalikira kosalekeza,
Ndidzayimbira zomlemekeza Mulungu wa Yakobo.
10Ndipo ndidzatseteka nyanga zonse za oipa;
Koma nyanga za wolungama zidzakwezeka.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Ulemerero ndi mphamvu ya Mulungu

Kwa Mkulu wa Nyimbo: pa Negtnolo. Salmo la Asafu. Nyimbo.

1Mulungu adziwika mwa Yuda:
Dzina lace limveka mwa Israyeli.
2Msasa wace unali m'Salemu, Ndipo pokhala Iye m'Ziyoni.
3Pomwepo anatyola mibvi ya paota;
Cikopa, ndi lupanga, ndi nkhondo.
4Inu ndinu wakuunikira, ndi womveka wakuposa mapiri muli acifwamba.
5Olimba mtima cifunkhidwa cuma cao, agona tulo tao;
Amuna onse amphamvu asowa manja ao.
6Pa kudzudzula kwanu, Mulungu wa Yakobo,
Gareta ndi kavalo yemwe anagwa m'tulo.
7Inu ndinu woopsa;
Ndipo utauka mkwiyo wanu adzakhala ciriri ndani pamaso panu?
8Mudamveketsa ciweruzo cocokera Kumwamba;
Dziko lapansi linacita mantha, nilinakhala cete,
9Pakuuka Mulungu kuti aweruze,
Kuti apulumutse ofatsa onse a pa dziko lapansi.
10Indedi, kuzaza kwace kwa munthu kudzakulemekezani;
Cotsalira ca kuzazaku mudzaciletsa.
11Windani ndipo citirani Yehova Mulungu wanu zowindazo;
Onse akumzinga abwere naco copereka ca kwa Iye amene ayenera kumuopa.
12Iye adzadula mzimu wa akulu;
Akhala woopsa kwa mafumu a pa dziko lapansi.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Acitankhawapokumbuka zocita Mulungu, koma alimbika mtima pokumbuka zina adazicita Iye

Kwa Mkulu wa Nyimbo; pa Yedutunu; Salmo la Asaru.

1 Ndidzapfuulira kwa Mulungu ndi mau anga;
Kwa Mulungu ndi mau anga, ndipo adzandicherezera khutu.
2 Tsiku la nsautso yanga ndinafuna Ambuye:
Dzanja langa linatambalika usiku, losaleka;
Mtima wanga unakanakutonthozedwa.
3 Ndikumbukila Mulungu ndipo ndibvutika;
Ndilingalira ndipo mzimu wanga ukomoka.
4 Mundikhalitsa maso;
Ndigwidwa mtima wosanena kanthu.
5 Ndinaganizira masiku akale, zaka zakalekale.
6 Ndikumbukila Nyimbo yanga, usiku;
Ndilingalira mumtima mwanga;
Mzimu wanga unasanthula.
7 Kodi Mulungu adzataya nthawi yonse?
Osabwerezanso kukondwera nafe.
8 Cifundo cace calekeka konse konse kodi?
Lonjezano lace lidatha kodi ku mibadwo yonse?
9 Kodi Mulungu waiwala kucita cifundo?
Watsekereza kodi nsoni zokoma zace mumkwiyo?
10 Ndipo ndinati, Cindilaka ici;
Koma ndikumbukila zaka za dzanja lamanja la
Wam'mwambamwamba.
11 Ndidzakumbukila zimene adazicita Ambuye;
Inde, ndidzakumbukila zodabwiza zanu zoyambira kale.
12 Ndipo ndidzalingalira nchito yanu yonse,
Ndi kulingalirabe zimene munazicita Inu.
13 Mulungu, m'malo opatulika muli njira yanu;
Mulungu wamkuru ndani monga Mulungu?
14 Inu ndinu Mulungu wakucita codabwiza;
Munazindikiritsa mphamvu yanu mwa mitundu ya anthu.
15 Munaombola anthu anu ndi mkonowanu,
Ndiwo ana a Yakobo, ndi a Yosefe.
16 Madziwo anakuonani Mulungu;
Anakuonani madziwo; anacita mantha:
Zozama zomwe zinanjenjemera,
17 Makongwa anatsanula madzi;
Thambo lidamvetsa liu lace;
Mibvi yanu yomwe inaturukira.
18 Liu la bingu lanu linatengezanatengezana;
Mphezi zinaunikira ponse pali anthu;

Dziko lapansi linanjenjemera ndi kugwedezeka.
19Njira yanu inali m'nyanja,
Koyenda Inu nku madzi akulu,
Ndipo mapazi anu sanadziwika.
20Munatsogolera anthu anu ngati gulu la nkhosa,
Ndi dzanja la Mose ndi Aroni,

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 78

Cikondi ndi cipiriro ca'Mulungu ca pa Aisrayeli osakhulupirika

Cilangizo ca Asatu.

1Tamverani, anthu anga, cilamulo canga;
Cherezani khutu lanu mau a pakamwa panga.
2Ndidzatsegula pakamwa panga mofanizira;
Ndidzachula zinsinsi zoyambira kale;
3Zimene tinazimva, ndi kuzidziwa,
Ndipo makolo athu anatifotokozera.
4Sitidzazibisira ana ao,
Koma kufotokozera mbadwo ukudzawo zolemekeza za Yehova,
Ndi mphamvu yace, ndi zodabwiza zace zimene anazicita.
5Anakhazika mboni mwa Yakobo,
Naika cilamulo mwa Israyeli,
Ndizo analamulira atate athu,
Akazidziwitse ana ao;
6Kuti mbadwo ukudzawo udziwe, ndiwo ana amene akadzabadwa;
Amene adzaimirira nadzafotokozera ana ao:
7Ndi kuti ciyembekezo cao cikhale kwa Mulungu,
Osaiwala zocita Mulungu,
Koma kusunga malamulo ace ndiko.
8Ndi kuti asange makolo ao,
Ndiwo mbadwo woukirana ndi wopikisana ndi Mulungu;
Mbadwo wosakonza mtima wao,
Ndi mzimu wao sunakhazikika ndi Mulungu.
9Ana a Efraimu okhala nazo zida, oponya nao mauta,
Anabwerera m'mbuyo tsiku la nkhondo.
10Sanasunga cipangano ca Mulungu,
Nakana kuyenda m'cilamulo cace.
11Ndipo anaiwala zocita Iye,
Ndi zodabwiza zace zimene anawaonetsa.
12Anacita codabwiza pamaso pa makolo ao,
M'dziko la Aigupto ku cidikha ca Zoanu.
13Anagawa nyanja nawapititsapo;
Naimitsa madziwo ngati khoma.
14Ndipo msana anawatsogolera ndi mtambo
Ndi usiku wonse ndi kuunika kwa moto.
15Anang'alula thanthwe m'cipululu,
Ndipo anawamwetsa kocuruka monga m'madzi ozama.
16Anaturukitsa mitsinje m'thanthwe,
Inde anatsikitsa madzi ngati mitsinje.
17Koma anaonjeza kuincimwira Iye,
Kupikisana ndi Wam'mwambamwamba m'cipululu.

18Ndipo anayesa Mulungu mumtimamwao
Ndi kupempha cakudya monga mwa kulakalaka kwao.
19Ndipo analankhula motsutsana ndi Mulungu;
Anati, Kodi Mulungu akhoza kutikonzera podyera m'cipululu?
20Taonani, anapanda thanthwe, ndi madzi anayendako
Ndi mitsinje inasefuka;
Kodi adzakhozanso kupatsa mkate?
Kodi adzafunira anthu ace nyama?
21Cifukwa cace Yehova anamva, nakwiya;
Ndipo anayatsa moto pa Yakobo,
Ndiponso mkwiyo unakwera pa Israyeli;
22Popeza sanakhulupirira Mulungu,
Osatama cipulumutso cace.
23Koma analamulira mitambo iri m'mwamba,
Natsegula m'makomo a kumwamba.
24Ndipo anawabvumbitsira mana, adye,
Nawapatsa tirigu wa kumwamba.
25Yense anadya mkate wa omveka:
Anawatumizira cakudya cofikira,
26Anaombetsa m'mwamba mphepo ya kum'mawa:
Natsogoza mwela ndi mphamvu yace.
27Ndipo anawabvumbitsira nyama ngati pfumbi,
Ndi mbalame zouluka ngati mcenga wa kunyanja:
28Ndipo anazigwetsa pakati pa misasa yao,
Pozungulira pokhala iwo.
29Potero anadya nakhuta kwambiri;
Ndipo anawapatsa cokhumba iwo.
30Asanathe naco cokhumba cao,
Cakudya cao ciri m'kamwa mwao,
31Pamenepo mkwiyo wa Mulungu unawaukira,
Ndipo anapha mwa onenepa ao,
Nagwetsa osankhika a Israyeli.
32Cingakhale ici conse anacimwanso,
Osabvomereza zodabwiza zace.
33Potero anathera masiku ao ndi zopanda pace,
Ndi zaka zao mwa mantha.
34Pamene anawapha ndipo anamfuna Iye;
Nabwerera, nafunitsitsa Mulungu,
35Ndipo anakumbukila kuti Mulungu ndiye thanthwe lao,
Ndi Mulungu Wam'mwambamwamba Mombolo wao.
36Koma anamsyasyalika pakamwa pao,
Namnamiza ndi lilime lao.
37Popeza mtima wao sunakonzekera Iye,
Ndipo sanakhazikika m'cipangano cace.

38Koma Iye pokhala ngwa cifundo,
Anakhululukira coipa, osawaononga;
Nabweza mkwiyo wace kawiri kawiri,
Sanautsa ukali wace wonse.
39Ndipo anakumbukira kuti iwo ndiwo anthu;
Mphepo yopita yosabweranso.
40Kawiri kawiri nanga anapikisana ndi Iye kucigwako,
Nammvetsa cisoni m'cipululu.
41Pakuti anabwerera m'mbuyo, nayesa Mulungu,
Nacepsa Woyerayo wa Israyeli.
42Sanakumbukila dzanja lace,
Tsikuli anawaombola kwa msautsi.
43Amene anaika zizindikilo zace m'Aigupto,
Ndi zodabwiza zace ku cidikha ca Zoanu;
44Nasanduliza nyanja yao mwazi,
Ndi mitsinje yao, kuti sangakhoze kumwa.
45Anawatumizira pakati pao mitambo ya nchenche zakuwatha;
Ndi acule akuwaononga.
46Ndipo anapatsa mphuci dzinthu dzao,
Ndi dzombe nchito yao.
47Anapha mphesa zao ndi matalala,
Ndi mikuyu yao ndi cisanu.
48Naperekanso zoweta zao kwa matalala,
Ndi ng'ombe zao kwa mphezi.
49Anawatumizira mkwiyo wace wotentha,
Kuzaza, ndi kupsa mtima, ndi nsautso,
Ndizo gulu la amithenga ocita zoipa.
50Analambulira mkwiyo wace njira;
Sanalekerera moyo wao usafe,
Koma anapereka moyo wao kumliri;
51Ndipo anapha ana oyamba onse a mu Aigupto,
Ndiwo oyamba a mphamvu yao m'mahema a Hamu:
52Koma anaturutsa anthu ace ngati nkhosa,
Nawatsogoza ngati gulu la zoweta m'cipululu.
53Ndipo anawatsogolera mokhulupirika,
Kotero kuti sanaopa;
Koma nyanja inamiza adani ao.
54Ndipo anawafikitsa ku malire a malo ace oyera,
Ku phiri ili, dzanja lamanja lace lidaligula.
55Ndipo anapitikitsa amitundu pamaso pao,
Nawagawira colowa cao, ndi muyeso,
Nakhalitsa mafuko a Israyeli m'mahema mwao.
56Koma anamuyesa napikisana ndi Mulungu
Wam'mwambamwamba,

Osasunga mboni zace;
57Koma anabwerera m'mbuyo, nacita zosakhulupirika monga
makolo ao:
Anapatuka ngati uta wolenda,
58Ndipo anautsa mtima wace ndi malo amsanje ao,
Namcititsa nsanje ndi mafano osema.
59Pakumva ici Mulungu, anakwiya, Nanyozatu Israyeli;
60Ndipo anacokera cokhalamo ca ku Silo,
Cihemaco adacimanga mwa anthu;
61Napereka mphamvu yace m'ukapolo,
Ndi ulemerero wace m'dzanja la msautsi.
62Naperekanso anthu ace kwa lupanga;
Nakwiya naco colandira cace.
63Moto unapsereza anyamata ao;
Ndi anamwali ao sanalemekezeka.
64Ansembe ao anagwa ndi lupanga;
Ndipo amasiye ao sanacita maliro.
65Pamenepo Ambuye anauka ngati wam'tulo;
Ngati ciphona cakucita nthungululu ndi vinyo.
66Ndipo anapanda otsutsana naye kumbuyo;
Nawapereka akhale otonzeka kosatha.
67Tero anakana hema wa Yosefe;
Ndipo sanasankha pfuko la Efraimu;
68Koma anasankha pfuko la Yuda,
Phiri la Ziyoni limene analikonda.
69Ndipo anamanga malo oyera ace ngati kaphiri,
Monga dziko lapansi limene analikhazikitsa kosatha.
70Ndipo anasankha Davide mtumiki wace,
Namtenga ku makola a nkhosa:
71Anamtenga kuja anatsata zoyamwitsa,
Awete Yakobo, anthu ace, ndi Israyeli, colandira cace.
72Potero anawaweta monga mwa mtima wace wangwiro;
Nawatsogolera ndi luso la manja ace.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Yerusalemu apasuka, apempha Mulungu awathandize

Salmo la Asafu.

1Mulungu, akunja alowa m'colandira canu;
Anaipsa Kacisi wanu woyera;
Anacititsa Yerusalemu bwinja.
2Anapereka mitembo ya atumiki anu ikhale cakudya ca mbalame za mlengalenga,
Nyama ya okondedwa anu anaipereka kwa zirombo za m'dziko.
3Anakhetsa mwazi wao ngati madzi pozungulira Yerusalemu;
Ndipo panalibe wakuwaika.
4Takhala cotonza ca anansi athu,
Ndi coseketsa ndi colalatitsa iwo akutizinga,
5Yehova, mudzakwiya nthawi zonse kufikira liti?
Nidzatentha nsanje yanu ngati moto?
6Thirirani mkwiyo wanu pa akunja osadziwa Inu,
Ndi pa maufumu osaitana pa dzina lanu.
7Pakuti anathera Yakobo,
Napasula pokhalira iye.
8Musakumbukile moritsutsa mphulupulu za makolo athu;
Nsoni zokoma zanu zitikumike msanga:
Pakuti tafoka kwambiri.
9Tithandizeni Mulungu wa cipulumutso cathu,
Cifukwa ca ulemerero wa dzina lanu;
Ndipo tilanditseni, ndi kutifafanizira zoipa zathu,
Cifukwa ca dzina lanu.
10Anenerenji amitundu, Ali kuti Mulungu wao?
Kubwezera cilango ca mwazi wa atumiki anu umene anaukhetsa
Kudziwike pakati pa amitundu pamaso pathu,
11Kubuula kwa wandende kufike kuli Inu;
Monga mwa mphamvu yanu yaikuru lolani ana a imfa atsale;
12Ndipo anansi athu amene anatonza Inu muwabwezere cotonza cao,
Kasanu ndi kawiri kumtima kwao, Ambuye.
13Potero ife anthu anu ndi nkhosa za pabusa panu
Tidzakuyamikani kosatha;
Tidzafotokozera cilemekezo canu ku mibadwo mibadwo.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 80

Apempha Mulungu alanditse anthu ace m'cisautso cao

Kwa Mkulu wa Nyimbo; pa Svosvantmuj locita mboni; Salmo la Asafu.

1Mbusa wa Israyeli, cherani khutu;
Inu wakutsogolera Yosefe ngati nkhosa;
Inu wokhala pa akerubi, walitsani.
2Utsani camuna canu pamaso pa Efraimu ndi Benjamini ndi Manase,
Ndipo mutidzere kutipulumutsa.
3Mutibweze, Mulungu;
Nimuwalitse nkhope yanu, ndipo tidzapulumuka.
4Yehova, Mulungu wa makamu,
Mudzakwiyira pemphero la anthu anu kufikira liti?
5Munawadyetsa mkate wa misozi,
Ndipo munawamwetsa misozi yambiri.
6Mutiika kuti atilimbirane anzathu;
Ndipo adani athu atiseka mwa iwo okha,
7Mulungu wa makamu, mutibweze;
Nimuwalitse nkhope yanu, ndipo tidzapulumuka.
8Mudatenga mpesa kucokera ku Aigupto:
Munapitikitsa amitundu ndi kuuoka uwu.
9Mudasoseratu pookapo,
Idagwiritsa mizu yace, ndipo unadzaza dziko.
10Mthunzi wace unaphimba mapiri,
Ndi nthambi zace zikunga mikungudza ya Mulungu.
11Unatambalitsa mphanda zace mpaka kunyanja,
Ndi mitsitsi yace kufikira ku Mtsinje.
12Munapasuliranii maphambo ace,
Kotero kuti onse akupita m'njira acherako?
13Nguruwe zocokera kuthengo ziukumba,
Ndi nyama za kucidikha ziudya,
14Bwererani, tikupemphani, Mulungu wa makamu;
Suzumirani muli m'mwamba, nimupenye, ndi kuzonda mpesa uwu,
15Ndi tsinde limene dzanja lanu lamanja linaokae
Ndi mphanda munadzilimbikitsira.
16Unapserera ndi moto, unadulidwa;
Aonongeka pa kudzudzula kwa nkhope yanu.
17Dzanja lanu likhale pa munthu wa pa dzanja lamanja lanu;
Pa mwana wa munthu amene munadzilimbikitsira.
18Potero sitidzabwerera m'mbuyo kukusiyani;
Titsitsimutseni, ndipo tidzaitanira dzina lanu.
19Mutibweze, Yehova Mulungu wa makamu;
Nimuwalitse nkhope yanu, ndipo tidzapulumuka.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 81

Mulungu atonza Aisrayeli pa kusamvera kwao

Kwa mkulu wa Nyimbo, pa Giliti. Salmo la Asafu.

1Yimbitsirani Mulungu ndiye mphamvu yathu;
Pfuulirani kwa Mulungu wa Yakobo.
2Utsani Salimo, bwera nakoni kalingaka,
Zeze wokondwetsa pamodzi ndi cisakasa.
3Ombani lipenga, pokhala mwezi,
Utakula mwezi, tsiku la phwando lathu.
4Pakuti ici ndi colemba ca kwa Israyeli,
Ciweruzo ca Mulungu wa Yakobo.
5Anaciika cikhale mboni kwa Yosefe,
Pakuturuka iye ku dziko la Aigupto:
Komwe ndinamva cinenedwe cosadziwa ine.
6Ndinamcotsera katundu paphewa pace:
Manja ace anamasuka kucotengera.
7Unaitana posautsika, ndipo ndinakulanditsa;
Ndinakubvomereza mobisalika m'bingu;
Ndinakuyesa ku madzi a Meriba.
8Tamvani, anthu anga, ndidzakucitirani mboni;
Israyeli, ukadzandimvera!
9Kwanu kusakhale mulungu wafuma kwina;
Nusagwadire mulungu wacilendo.
10Ine ndine Yehova Mulungu wako amene ndinakukweza kukucotsa ku dziko la Aigupto;
Yasamitsa pakamwa pako ndipo ndidzalidzaza.
11Koma anthu anga sanamvera mau anga;
Ndipo Israyeli sanandibvomera.
12Potero ndinawaperekera kuuma mtima kwao,
Ayende monga mwa uphungu wao wao.
13Ha! akadandimvera anthu anga,
Akadayenda m'njira zanga Israyeli!
14Ndikadagonjetsa adani ao msanga,
Ndikadabweza dzanja langa pa owasautsa.
15Akumuda Yehova akadamgonjera mungakhale monyenga:
Koma nyengo yao ikadakhala yosatha,
16Akadawadyetsa naye tirigu wakometsetsa:
Ndikadakukhutitsanso ndi uci wa m'thanthwe.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 82

Oweruza aweruze bwino

Salmo la Asatu.

1Mulungu aima mu msonkhano wa Mulungu,
Aweruza pakati pa milungu.
2Mudzaweruza mosalunjika kufikira liti,
Ndi kusamalira nkhope ya oipa?
3Weruzani osauka ndi amasiye;
Weruzani molungama ozunzika ndi osowa.
4Pulumutsani osauka ndi aumphawi:
Alanditseni m'dzanja la oipa,
5Sadziwa, ndipo sazindikira;
Amayendayenda mumdima;
Maziko onse a dziko lapansi agwedezeka.
6Ndinati Ine, Inu ndinu milungu,
Ndi ana a Wam'mwambamwamba nonsenu.
7Komatu mudzafa monga anthu,
Ndipo mudzagwa monga wina wa akulu.
8Ukani, Mulungu, weruzani dziko lapansi;
Pakuti Inu mudzalandira amitundu onse.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 83

Amitundu apangana kuononga Aisrayeli, Apempha Mulungu awalanditse

Nyimbo. Satmo la Asatu.

1Mulungu musakhale cete;
Musakhale du, osanena kanthu, Mulungu.
2Pakuti taonani, adani anu aphokosera:
Ndipo okwiyira Inu aweramutsa mutu,
3Apangana mocenjerera pa anthu anu,
Nakhalira upo pa obisika anu.
4Amati, Tiyeni tiwaononge asakhalenso mtundu wa anthu;
Ndipo dzina la Israyeli lisakumbukikenso.
5Pakuti anakhalira upo ndi mtima umodzi;
Anacita cipangano ca pa Inu:
6Mahema a Edomu ndi a Aismayeli;
Moabu ndi Ahagara;
7Gebala ndi Amoni ndi Amaleki;
Filistiya, pamodzi ndi iwo okhala m'Turo.
8Asuri anaphatikana nao;
Anakhala dzanja la ana a Loti,
9Muwacitire monga munacitira Midyani;
Ndi Sisera, ndi Jabini ku mtsinje wa Kisoni:
10Amene anaonongeka ku Endoro;
Anakhala ngati ndowe ya kumunda.
11Muwaike akulu ao ngati Orebu ndi Zeebu;
Mafumu ao ngati Zeba ndi Zalimuna:
12Amene anati, Tilande
Malo okhalamo Mulungu, akhale athu.
13Mulungu wanga, muwaike akhale ngati mungu;
Ngati ziputu zomka ndi mphepo.
14Monga moto upsereza nkhalango,
Ndi monga lawi liyatsa mapiri;
15Momwemo muwatsate ndi namondwe,
Nimuwaopse ndi kabvumvulu wanu.
16Acititseni manyazi pankhope pao;
Kuti afune dzina lanu, Yehova.
17Acite manyazi, naopsedwe kosatha;
Ndipo asokonezeke, naonongeke:
18Kuti adziwe kuti inu nokha, dzina lanu ndinu Yehova,
Ndinu Wam'mwambamwamba pa dziko lonse lapansi.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 84

Okhala m'nyumba ya Yehova ndiwo amwai

Kwa Mkulu wa Nyimbo, pa Gitili: Salmo la ana a Kora.

1Pokhala Inu mpotikonda ndithu, Yehova wa makamu!
2Moyo wanga ulakalaka, inde ukomokanso ndi kufuna mabwalo a Yehova;
Mtima wanga ndi thupi langa zipfuulira kwa Mulungu wamoyo.
3Mbawanso inapeza nyumba,
Ndi namzeze cisa cace coikamo ana ace,
Pa maguwa a nsembe anu, Yehova wa makamu,
Mfumu yanga ndi Mulungu wanga,
4Odala iwo akugonera m'nyumba mwanu;
Akulemekezani cilemekezere,
5Wodala munthu amene mphamvu yace iri mwa Inu;
Mumtima mwace muli makwalala a ku Ziyoni,
6Popyola cigwa ca kulira misozi aciyesa ca akasupe;
Inde mvula: ya cizimalupsa icidzaza ndi madalitso.
7Apita mwamphamvu naonjezapo mphamvu,
Aoneka pamaso pa Mulungu m'Ziyoni.
8Yehova Mulungu wa makamu, imvani pemphero langa:
Cherani khutu, Mulungu wa Yakobo.
9Onani, Mulungu, ndinu cikopa cathu;
Ndipo penyani pa nkhope ya Wodzozedwa wanu.
10Pakuti tsiku limodzi m'mabwalo anu likoma koposa masiku ambirimbiri akukhala pena,
Kukhala inewapakhomo m'nyumba ya Mulungu wanga,
Kundikonda ine koposa kugonera m'mahema a coipa,
11Pakuti Yehova Mulungu ndiye dzuwa ndi cikopa;
Yehova adzapatsa cifundo ndi ulemerero;
Sadzakaniza cokoma iwo akuyenda angwiro,
12Yehova wa makamu,
Wodala munthu wakukhulupirira Inu.

Masalmo 85

Akumbutsa Mulungu madalitso akale, apempha awabwereze

Kwa Mkulu wa Nyimbo: Satmo la ana a Kora.

1 Munacita zobvomereza dziko lanu, Yehova;
Munabweza ukapolo wa Yakobo.
2 Munacotsa mphulupulu ya anthu anu,
Munafotsera zolakwa zao zonse.
3 Munabweza kuzaza kwanu konse;
Munabwerera ku mkwiyo wanu wotentha.
4 Mutibweze, Mulungu wa cipulumutso cathu,
Nimuletse udani wanu wa pa ife.
5 Kodi mudzatikwiyira nthawi zonse?
Kodi mudzakhala cikwiyire mibadwo mibadwo?
6 Kodi simudzatipatsanso moyo,
Kuti anthu anu akondwerere ndi Inu?
7 Tionetseni cifundo canu, Yehova,
Tipatseni cipulumutso canu.
8 Ndidzamva colankhula Mulungu Yehova;
Pakuti adzalankhula zamtendere ndi anthu ace, ndi okondedwa ace;
Koma asabwererenso kucita zapusa.
9 Indedi cipulumutso cace ciri pafupi ndi iwo akumuopa Iye;
Kuti m'dziko mwathu mukhale ulemu.
10 Cifundo ndi coonadi zakomanizana;
Cilungamo ndi mtendere zapsompsonana,
11 Coonadi ciphukira m'dziko;
Ndi cilungamo casuzumira ciri m'mwamba.
12 Inde Yehova adzapereka zokoma;
Ndipo dziko lathu lidzapereka zipatso zace.
13 Cilungamo cidzamtsogolera; Nicidzamkonzera mapazi ace njira.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 86

Davide apempha Mulungu kolimba amlanditse

Pemphero la Davide.

1Cherani khutu lanu Yehova, mundiyankhe;
Pakuti ine ndine wozunzika ndi waumphawi.
2Sungani moyo wanga pakuti ine ndine wokondedwa wanu;
Inu Mulungu wanga, pulumutsani mtumiki wanu wokhulupirira Inu.
3Mundicitire cifundo, Ambuye;
Pakuti tsiku lonse ndiitana Inu.
4Kondwetsani moyo wa mtumiki wanu;
Pakuti ndikwezera moyo wanga kwa Inu, Ambuye.
5Pakuti fnu, Ambuye, ndinu wabwino, ndi wokhululukira,
Ndi wa cifundo cocurukira onse akuitana Inu.
6Cherani khutu pemphero langa, Yehova;
Nimumvere mau a kupemba kwanga,
7Tsiku la msauko wanga ndidzaitana Inu;
Popeza mudzandibvomereza.
8Pakati pa milungu palibe wina wonga Inu, Ambuye;
Ndipo palibe nchito zonga zanu.
9Amitundu onse mudawalenga adzadza nadzagwada pamaso panu,
Ambuye; Nadzalemekeza dzina lanu.
10Pakuti Inu ndinu wamkulu, ndi wakucita zodabwiza;
Inu ndinu Mulungu, nokhanu.
11Mundionetse njira yanu, Yehova; ndidzayenda m'coonadi canu:
Muumbe mtima wanga ukhale umodzi kuti uliope dzina lanu.
12Ndidzakuyamikani, Ambuye, Mulungu wanga, ndi mtima wanga wonse;
Ndipo ndidzalemekeza dzina lanu nthawi zonse.
13Pakuti cifundo canu ca pa ine ncacikuru;
Ndipo munalanditsa moyo wanga kunsi kwa manda.
14Mulungu, odzikuza andiukira,
Ndi msonkhano wa anthu oopsa afuna moyo wanga,
Ndipo sanaika Inu pamaso pao.
15Koma Inu, Ambuye, ndinu Mulungu wansoni ndi wacisomo,
Wosapsa mtima msanga, ndi wocurukira cifundo ndi coonadi.
16Mundibwerere ine, ndi kundicitira cifundo;
Mpatseni mtumiki wanu mphamvu yanu,
Ndipo pulumutsani mwana wa mdzakazi wanu.
17Mundicitire cizindikilo coti cabwino;
Kuti ondida acione, nacite manyazi,
Popeza Inu, Yehova, munandithandiza ndi kundisangalatsa,

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 87

Yehova akonda Ziyoni

Salmo la ana a Kora: Nyimbo.

1Maziko ace ali m'mapiri oyera.
2Yehova akonda zipata za Ziyoni
Koposa zokhalamo zonse za Yakobo.
3Mudzi wa Mulungu, inu,
Akunenerani zakukulemekezani.
4Ndidzachula Rahabu ndi Babulo kwa iwo ondidziwa Ine;
Taonani, Filistiya ndi Turo pamodzi ndi Kusi;
Uyu anabadwa komweko.
5Ndipo adzanena za Ziyoni,
Uyu ndi uyo anabadwa m'mwemo;
Ndipo Wam'mwambamwamba ndiye aclzaukhazikitsa.
6Yehova adzawerenga, polembera mitundu ya anthu.
Uyu anabadwa komweko.
7Ndipo oyimba ndi oomba omwe adzati,
Akasupe ansa onse ali mwa inu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Wa Salmo achula masautso ace, napempha Mulungu amdalitse kuimfa

Nyimbo. Salmo la ana a Kora. Kwa Mkulu wa Nyimbo, pa Mahalata Leanotu. Cilangizo ca Hemana M-ezara.

1Yehova, Mulungu wa cipulumutso canga,
Ndinapfuula pamaso panu usana ndi usiku,
2Pemphero langa lidze pamaso panu;
Mundicherere khutu kukuwa kwanga:
3Pakuti mzimu wanga wadzala nao mabvuto,
Ndi moyo wanga wayandikira kumanda.
4Anandiwerenga pamodzi nao otsikira kudzenje;
Ndakhala ngati munthu wopanda mphamvu:
5Wotayika pakati pa akufa,
Ngati ophedwa akugona m'manda,
Amene simuwakumbukilanso;
Ndipo anawadula kusiyana ndi dzanja lanu.
6Munandiika kunsi kwa dzenje,
Kuti mdima, kozama.
7Mkwiyo wanu utsamira pa ine,
Ndipo munandizunza ine ndi mafunde anu onse.
8Munandisiyanitsira wodziwana nane kutali;
Munandiika ndiwakhalire conyansa:
Ananditsekereza osakhoza kuturuka ine.
9Diso langa lapuwala cifukwa ca kuzunzika kwanga:
Ndimaitana Inu, Yehova, tsiku lonse;
Nditambalitsira manja anga kwa Inu.
10Kodi mudzacitira akufa zodabwiza?
Kodi adzaukanso otisiyawo, ndi kukulemekezani?
11Adzafotokozera cifundo canu kumanda kodi,
Cikhulupiriko canu ku malo a cionongeko?
12Zodabwiza zanu zidzadziwika mumdima kodi,
Ndi cilungamo canu m'dziko la ciiwaliko?
13Koma ndinapfuulira kwa Inu, Yehova,
Ndipo pemphero langa likumika Inu mamawa.
14Yehova mutayiranji moyo wanga?
Ndi kundibisira nkhope yanu?
15Wozunzika ine ndi wofuna kufa kuyambira ubwana wanga;
Posenza zoopsa zanu, ndithedwa nzeru.
16Kuzaza kwanu kwandimiza;
Zoopsa zanu zinandiononga,
17Zinandizungulira ngati madzi tsiku lonse;
Zinandizinga pamodzi.
18Munandicotsera kutali wondikonda ndi bwenzi langa,

Odziwana nane akhala kumdima.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 89

Pangano la Mulungu ndi Davide. Mulungu adzapulumutsa anthu ace

Cilangizo ca Etana M-ezera.

1Ndidzayimbira zacifundo za Yehova nthawi yonse:
Pakamwa panga ndidzadziwitsira cikhulupiriko canu ku mibadwo mibadwo.
2Pakuti ndinati, Cifundo adzacimanga kosaleka;
Mudzakhazika cikhulupiriko canu m'Mwamba mweni mweni.
3Ndinacita cipangano ndi wosankhika wanga,
Ndinalumbirira Davide mtumiki wanga:
4Ndidzakhazika mbeu yako ku nthawi yonse,
Ndipo ndidzamanga mpando wacifumu wako ku mibadwo mibadwo.
5Ndipo kumwamba kudzalemekeza zodabwiza zanu, Yehova;
Cikhulupiriko canunso mu msonkhano wa oyera mtima.
6Pakuti kuli yani kuthambo timlinganize ndi Yehova?
Afanana ndi Yehova ndani mwa ana a amphamvu?
7Ndiye Mulungu, ayenera kumuopa kwambiri m'upo wa oyera mtima,
Ndiye wocititsa mantha koposa onse akumzinga.
8Yehova, Mulungu wa makamu, wamphamvu ndani wonga Inu, Yehova?
Ndipo cikhulupiriko canu cikuzingani.
9Inu ndinu wakucita ufumu pa kudzikuza kwa nyanja;
Pakuuka mafunde ace muwacititsa bata.
10Mudathyola Rahabu, monga munthu wophedwa;
Munabalalitsa adani anu ndi mkono wa mphamvu yanu.
11Kumwamba ndi kwanu, dziko lapansi lomwe ndi lanu;
Munakhazika dziko lokhalamo anthu ndi kudzala kwace.
12Munalenga kumpoto ndi kumwela;
Tabora ndi Hermoni apfuula mokondwera m'dzina lanu.
13Muli nao mkono wanu wolimba;
M'dzanja mwanu muli mphamvu, dzanja lamanja lanu nlokwezeka.
14Cilungamo ndi ciweruzo ndiwo maziko a mpando wacifumu wanu;
Cifundo ndi coonadi zitsogolera pankhope panu.
15Odala anthu odziwa liu la lipenga;
Ayenda m'kuunika kwa nkhope yanu, Yehova.
16Akondwera m'dzina lanu tsiku lonse;
Ndipo akwezeka m'cilungamo canu.
17Popeza Inu ndinu ulemerero wa mphamvu yao;
Ndipo potibvomereza Inu nyanga yathu idzakwezeka.
18Pakuti cikopa cathu cifuma kwa Yehova;
Ndi mfumuyathu kwa Woyera wa Israyeli.
19Pamenepo munalankhula m'masompenya ndi okondedwa anu,

Ndipo mudati, Ndasenza thandizo pa ciphona;
Ndakweza wina wosankhika mwa anthu.
20Ndapeza Davide mtumiki wanga;
Ndamdzoza mafuta anga oyera.
21Amene dzanja langa lidzakhazikika naye;
Inde mkono wanga udzalimbitsa.
22Mdani sadzamuumira mtima;
Ndi mwana wa cisalungamo sadzamzunza.
23Ndipo ndidzaphwanya omsautsa pamaso pace;
Ndidzapandanso odana naye.
24Koma cikhulupiriko canga ndi cifundo canga zidzakhala naye;
Ndipo nyanga yace idzakwezeka m'dzina langa.
25Ndipo ndidzaika dzanja lace panyanja,
Ndi dzanja lamanja lace pamitsinje.
26Iye adzandichula, ndi kuti, Inu ndinu Atate wanga,
Mulungu wanga, ndi thanthwe la cipulumutso canga.
27Inde ndidzamuyesa mwana wanga woyamba,
Womveka wa mafumu a pa dziko lapansi.
28Ndidzamsungira cifundo canga ku nthawi yonse,
Ndipo cipangano canga cidzalimbika pa iye.
29Ndidzakhalitsanso mbeu yace cikhalire,
Ndi mpando wacifumu wace ngati masiku a m'mwamba.
30Ana ace akataya cilamulo canga,
Osayenda m'maweruzo anga:
31Nakaipsa malembo anga;
Osasunga malamulo anga;
32Pamenepo ndidzazonda zolakwa zao ndi ndodo,
Ndi mphulupulu zao ndi mikwingwirima.
33Koma sindidzamcotsera cifundo canga conse,
Ndi cikhulupiriko canga sicidzamsowa.
34Sindidzaipsa cipangano canga,
Kapena kusintha mau oturuka m'milomo yanga.
35Ndinalumbira kamodzi m'ciyero canga;
Sindidzanamizira Davide;
36Mbeu yace idzakhala ku nthawi yonse,
Ndi mpando wacifumu wace ngati dzuwa pamaso panga.
37Udzakhazikika ngati mwezi ku nthawi yonse,
Ndi ngati mboni yokhulupirika kuthambo.
38Koma Inu munamtaya, nimunamkaniza,
Munakwiya naye wodzozedwa wanu.
39Munakaniza cipangano ca mtumiki wanu;
Munaipsa korona wace ndi kumponya pansi,
40Munapasula maguta ace onse;
Munagumula malinga ace.

41Onse opita panjirapa amfunkhira:
Akhala cotonza ca anansi ace.
42Munakweza dzanja lamanja la iwo omsautsa;
Munakondweretsa adani ace onse.
43Munapinditsa kukamwa kwace kwa lupanga lace,
Osamuimika kunkhondo.
44Munaleketsa kuwala kwace,
Ndipo munagwetsa pansi mpando wacifumu wace.
45Munafupikitsa masiku a mnyamata wace;
Munamkuta nao manyazi.
46Mudzabisala kosatha kufikira liti, Yehova;
Ndi kuzaza kwanu kudzatentha ngati moto kufikira liti?
47Kumbukilani kuti nthawi yanga njapafupi;
Munalengeranji ana onse a anthu kwacabe?
48Munthu ndani amene adzakhalabe ndi moyo, osaona imfa?
Amene adzapulumutsa moyo wace ku mphamvu ya manda?
49Ciri kuti cifundo canu cakale, Ambuye,
Munacilumbirira Davide pa cikhulupiriko canu?
50Kumbukilani, Ambuye, cotonzera atumiki anu;
Ndicisenza m'cifuwa mwanga cacokera ku mitundu yonse yaikuru ya anthu;
51Cimene adani anu, Yehova, atonza naco;
Cimene atonzera naco mayendedwe a wodzozedwa wanu.
52Wodalitsika Yehova ku nthawi yonse,
Amen ndi Amen.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 90

Mulungu ndiye wacikhalire, munthu ndiye wakutha msanga

Pemphero la Mose munthu wa Mulungu.

1Ambuye, Inu munatikhalira mokhalamo
M'mibadwo mibadwo.
2Asanabadwe mapiri,
Kapena musanalenge dziko lapansi, ndi lokhalamo anthu,
Inde, kuyambira nthawi yosayamba kufikira nthawi yosatha,
Inu ndinu Mulungu.
3Mubweza munthu akhale pfumbi;
Nimuti, Bwererani inu, ana a anthu.
4Pakuti pamaso panu zaka zikwi
Zikhala ngati dzulo, litapita,
Ndi monga ulonda wa usiku.
5Muwatenga ngati ndi madzi akulu, akhala ngati tulo;
Mamawa akhala ngati msipu waphuka.
6Mamawa uphuka bwino;
Madzulo ausenga, nuuma.
7Pakuti tiononge ka mu mkwiyo wanu;
Ndipo m'kuzaza kwanu tiopsedwa.
8Munaika mphulupulu zathu pamaso panu,
Ndi zoipa zathu zobisika pounikira nkhope yanu.
9Pakuti masiku athu onse apitirira m'ukali wanu;
Titsiriza moyo wathu ngati lingaliro.
10Masiku a zaka zathu ndiwo zaka makumi asanu ndi awiri,
Kapena tikakhala nayo mphamvudi zaka makumi asanu ndi atatu;
Koma teronso kukula kwao kumati cibvuto ndi copanda pace;
Pakuti kumapitako msanga ndipo tithawa ife tomwe.
11Adziwa mphamvu ya mkwiyo wanu ndani,
Ndi ukali wanu monga ayenera kukuopani?
12Mutidziwitse kuwerenga masiku athu motero,
Kuti tikhale nao mtima wanzeru.
13Bwerani, Yehova; kufikira liti?
Ndipo alekeni atumiki anu.
14Mutikhutitse naco cifundo canu m'mawa;
Ndipo tidzapfuula mokondwera ndi kukondwera masiku athu onse.
15Tikondweretseni monga mwa masiku mudatizunzawa,
Ndi zaka tidaona coipa.
16Cocita Inu cioneke kwa atumiki anu,
Ndi ulemerero wanu pa ana ao.
17Ndipo cisomo cace ca Yehova Mulungu wathu cikhale pa ife;
Ndipo mutikhazikitsire ife nchito ya manja athu;
Inde, nchito ya manja athu muikhazikitse.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 91

Mulungu asungadi wodzipereka kwa Iye

1Iye amene akhala pansi m'ngaka yace ya Wam'mwambamwamba
Adzagonera mu mthunzi wa Wamphamvuyonse.
2Ndidzati kwa Yehova, Pothawirapo panga ndi linga langa;
Mulungu wanga, amene ndimkhulupirira,
3Pakuti adzakuonjola ku msampha wa msodzi,
Ku mliri wosakaza.
4Adzakufungatira ndi nthenga zace,
Ndipo udzathawira kunsi kwa mapiko ace;
Coonadi cace ndico cikopa cocinjiriza.
5Sudzaopa coopsa ca usiku, Kapena mubvi wopita usana;
6Kapena mliri woyenda mumdima,
Kapena cionongeko cakuthera usana.
7Pambali pako padzagwa cikwi,
Ndi zikwi khumi pa dzanja lamanja lako;
Sicidzakuyandikiza iwe.
8Koma udzapenya ndi maso ako,
Nudzaona kubwezera cilango oipa.
9Popeza udati, Inu Yehova, ndinu pothawirapo panga
Udaika Wam'mwambamwamba cokhalamo cako;
10Palibe coipa cidzakugwera,
Ndipo colanga sicidzayandikiza hema wako.
11Pakuti adzalamulira angelo ace za iwe,
Akusunge m'njira zako zonse.
12Adzakunyamula pa manja ao,
Ungagunde phazi lako pamwala.
13Udzaponda mkango ndi mphiri;
Udzapondereza msona wa mkango ndi cinjoka:
14Popeza andikondadi ndidzampulumutsa;
Ndidzamkweza m'mwamba, papeza adziwa dzina langa.
15Adzandipfuulira Ine ndipo ndidzamyankha;
Kunsautso ndidzakhala naye pamodzi;
Ndidzamlanditsa, ndi kumcitira ulemu.
16Ndidzamkhutitsa ndi masiku ambiri,
Ndi kumuonetsera cipulumutso canga,

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 92

Anthu onse ayamike Mulungu cifukwa ca nchito zace, cilungamo cace, ndi cifundo cace

Satmo, Nyimbo ya pa Sabata,

1Nkokoma kuyamika Yehova,
Ndi kuyimbira nyimbo dzina lanu, Wam'mwambamwamba Inu:
2Kuonetsera cifundo canu mamawa,
Ndi cikhulupiriko canu usiku uli wonse.
3Pa coyimbira ca zingwe khumi ndi pacisakasa;
Pazeze ndi kulira kwace.
4Popeza Inu, Yehova, munandikondweretsa ndi kucita kwanu,
Ndidzapfuula mokondwera pa nchito ya manja anu.
5Ha! nchito zanu nzazikuru, Yehova,
Zolingalira zanu nzozama ndithu.
6Munthu wopulukira sacidziwa;
Ndi munthu wopusa sacizindikira ici;
7Cakuti pophuka oipa ngati msipu,
Ndi popindula ocita zopanda pace;
Citero kuti adzaonongeke kosatha:
8Koma Inu, Yehova, muli m'mwamba ku nthawi yonse.
9Pakuti, taonani, adani anu, Yehova,
Pakuti, taonani, adani anu adzatayika;
Ocita zopanda pace onse adzamwazika.
10Koma munakweza nyanga yanga ngati ya njati;
Anandidzoza mafuta atsopano.
11Diso langa lapenya cokhumba ine pa iwo ondilalira,
M'makutu mwanga ndamva cokhumba ine pa iwo akucita zoipa akundiukira.
12Wolungama adzaphuka ngati mgwalangwa;
Adzakula ngati mkungudza wa ku Lebano.
13Iwo ookedwa m'nyumba ya Yehova,
Adzaphuka m'mabwalo a Mulungu wathu.
14Atakalamba adzapatsanso zipatso;
Adzadzazidwa ndi madzi nadzakhala abiriwiri:
15Kulalikira kuti Yehova ngwolunjika;
Iye ndiye thanthwe langa, ndipo mwa Iye mulibe cosalungama.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 93

Ufumu wa Mulungu ndiwo wa ulemerero, mphamvu, ndi ciyero

1Yehova acita ufumu; wadzibveka ndi ukulu;
Wadzibveka Yehova, wadzimangirira mphamvu m'cuuno;
Dziko lomwe lokhalamo anthu likhazikika, silidzagwedezeka.
2Mpando wacifumu wanu ukhazikika kuyambira kale lija;
Inu ndinu wosayambira ndi kale, lomwe.
3Mitsinje ikweza, Yehova,
Mitsinje ikweza mkokomo wao;
Mitsinje ikweza mafunde ao.
4Yehova Wam'mwamba ndiye wamphamvu,
Wakuposa mkokomo wa madzi ambiri,
Ndi mafunde olimba a nyanja.
5Mboni zanu zibvomerezeka ndithu;
Ciyero ciyenera nyumba yanu, Yehova, ku nthawi za muyaya.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 94

Mulungu wolungama adzaweruza otpa

1Mulungu wakubwezera cilango,
Yehova, Mulungu wakubwezera cilango, muoneke wowala.
2Nyamukani, Inu woweruza wa dziko lapansi:
Bwezerani odzikuza coyenera iwo.
3Oipa adzatumpha ndi cimwemwe kufikira liti, Yehova?
Oipa adzatero kufikira liti?
4Anena mau, alankhula zawawa;
Adzitamandira onse ocita zopanda pace.
5Aphwanya anthu anu, Yehova,
Nazunza colandira canu.
6Amapha wamasiye ndi mlendo,
Nawapha ana amasiye.
7Ndipo amati, Yehova sacipenya,
Ndi Mulungu wa Yakobo sacisamalira.
8Zindikirani, opulukira inu mwa anthu;
Ndipo opusa inu, mudzacita mwanzeru liti?
9Kodi Iye wakupanga khutu ngwosamva?
Kodi Iye wakuumba diso ngwosapenya?
10Kodi Iye wakulangiza mitundu ya anthu, ndiye wosadzudzula?
Si ndiye amene aphunzitsa munthu nzeru?
11Yehova adziwa zolingalira za munthu,
Kuti ziri zacabe.
12Wodala munthu amene mumlanga, Yehova;
Ndi kumphunzitsa m'cilamulo canu;
13Kuti mumpumitse masiku oipa;
Kufikira atakumbira woipa mbuna.
14Pakuti Yehova sadzasiya anthu ace,
Ndipo sadzataya colandira cace.
15Pakuti ciweruzo cidzabwera kumka kucilungamo:
Ndipo oongoka mtima onse adzacitsata.
16Adzandiukira ndani kutsutsana nao ocita zoipa?
Adzandilimbikira ndani kutsutsana nao ocita zopanda pace?
17Akadapanda kukhala thandizo langa Yehova,
Moyo wanga ukadakhala kuli cete.
18Pamene ndinati, Litereka phazi langa,
Cifundo canu, Mulungu, cinandicirikiza.
19Pondicurukira zolingalira zanga m'kati mwanga,
Zotonthoza zanu zikondweretsa moyo wanga.
20Kodi uyenera kuyanjana ndi Inu mpando wacifumu wa kusakaza,
Wakupanga cobvuta cikhale lamulo?
21Asonkhana pamodzi pa moyo wa wolungama,
Namtsutsa wa mwazi wosacimwa.

22Koma Yehova wakhala msanje wanga;
Ndi Mulungu wanga thanthwe lothawirapo ine.
23Ndipo anawabwezera zopanda pace zao,
Nadzawaononga m'coipa cao;
Yehova Mulungu wathu adzawaononga.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 95

Adandaulira anthu alemekeze namvere Mulungu wao wamkuru

1Tiyeni tiyimbire Yehova mokondwera;
Tipfuule kwa thanthwe la cipulumutso cathu.
2Tidze naco ciyamiko pamaso pace,
Timpfuulire Iye mokondwera ndi masalmo.
3Pakuti Yehova ndiye Mulungu wamkuru;
Ndi mfumu yaikuru yoposa milungu yonse.
4Malo ozama a dziko lapansi ali m'dzanja lace;
Cuma ca m'mapiri comwe ndi cace.
5Nyanja ndi yace, anailenga;
Ndipo manja ace anaumba dziko louma.
6Tiyeni, tipembedze tiwerame;
Tigwade pamaso pa Yehova, amene anatilenga:
7Pakuti Iye ndiye Mulungu wathu,
Ndipo ife ndife anthu a pabusa pace, ndi nkhosa za m'dzanja mwace.
Lero, mukamva mau acel
8Musaumitse mitima yanu, ngati ku Meriba,
Ngati tsiku la ku Masa m'cipululu;
9Pamene makolo anu anandisuntha,
Anandiyesa, anapenyanso cocita Ine.
10Zaka makumi anai mbadwo uwu unandimvetsa cisoni,
Ndipo ndinati, Iwo ndiwo anthu osokerera mtima,
Ndipo sadziwa njira zanga.
11Cifukwa cace ndinalumbira mu mkwiyo wanga,
Ngati adzalowa mpumulo wanga.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 96

Onse a pansi pano ndi am'mwamba omwe alemekeze Mulungu

1Myimbireni Yehova nyimbo yatsopano;
Myimbireni Yehova, inu, dziko lonse lapansi.
2Myimbireni Yehova, lemekezani dzina lace;
Lalikirani cipulumutso cace tsiku ndi tsiku.
3Fotokozerani ulemerero wace mwa amitundu;
Zodabwiza zace mwa mitundu yonse ya anthu.
4Pakuti Yehova ndi wamkulu, nayenera kulemekezedwa kwakukulu;
Ayenera amuope koposa milungu yonse.
5Pakuti milungu yonse ya mitundu ya anthu ndiyo mafano:
Koma Yehova analenga zakumwamba.
6Pamaso pace pali ulemu ndi ukulu:
M'malo opatulika mwace muli mphamvu ndi zocititsa kaso.
7Mpatseni Yehova, inu, mafuko a mitundu ya anthu,
Mpatseni Yehova ulemerero ndi mphamvu,
8Mpatseni Yehova ulemerero wa dzina lace;
Bwerani naco copereka, ndipo fikani ku mabwalo ace.
9Gwadirani Yehova moyera ndi mokometsetsa:
Njenjemerani pamaso pace, inu dziko lonse lapansi.
10Nenani mwa amitundu, Yehova acita ufumu;
Dziko lokhalamo anthu lomwe likhazikika kuti silingagwedezeke;
Adzaweruza mitundu ya anthu molunjika.
11Kumwamba kukondwere nilisekerere dziko lapansi;
Nyanja ibume mwa kudzala kwace:
12Munda ukondwerere ndi zonse ziri m'mwemo;
Pamenepo mitengo yonse ya kunkhalango idzapfuula mokondwera;
13Pamaso pa Yehova, pakuti akudza;
Pakuti akudza kudzaweruza dziko lapansi:
Adzaweruza dziko lokhalamo anthu ndi cilungamo,
Ndi mitundu ya anthu ndi coonadi.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 97

Ulemerero wa ufumu wa Mulungu

1Yehova acita ufumu; dziko lapansi likondwere;
Zisumbu zambiri zikondwerere.
2Pomzinga pali mitambo ndi mdima;
Cilungamo ndi ciweruzo ndizo zolimbitsa mpando wacifumu wace.
3Moto umtsogolera,
Nupsereza otsutsana naye pozungulirapo,
4Mphezi zace zinaunikira dziko lokhalamo anthu;
Dziko lapansi linaona nilinagwedezeka.
5Mapiri anasungunuka ngati sera pamaso pa Yehova,
Pamaso pa Ambuye wa dziko lonse lapansi.
6Kumwamba kulalikira cilungamo cace,
Ndipo mitundu yonse ya anthu ipenya ulemerero wace.
7Onse akutumikira fano losema,
Akudzitamandira nao mafano, acite manyazi:
Mgwadireni Iye, milungu yonse inu.
8Ziyoni anamva nakondwera,
Nasekerera ana akazi a Yuda;
Cifukwa ca maweruzo anu, Yehova.
9Pakuti Inu, Yehova, ndinu Wam'mwambamwamba pa dziko lonse lapansi,
Ndinu wokwezeka kwakukuru pamwamba pa milungu yonse yina.
10Inuokonda Yehova, danani naco coipa:
Iye asunga moyo wa okondedwa ace;
Awalanditsa m'manja mwa oipa.
11Kuunika kufesekera wolungama, Ndi cikondwerero oongoka mtima.
12Kondwerani mwa Yehova, olungama inu;
Ndipo yamikani pokumbukila ciyero cace.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 98

Alemekeze Mulungu pa cifundo ndi coonadi cao

Sa1mo.

1Myimbireni Yehova nyimbo yatsopano;
Popeza anacita zodabwiza:
Dzanja lace lamanja, mkono wace woyera, zinamcitira cipulumutso,
2Yehova anawadziwitsira cipulumutso cace;
Anaonetsera cilungamo cace pamaso pa amitundu.
3Anakumbukila cifundo cace ndi cikhulupiriko cace ku nyumba ya Israyeli;
Malekezero onse a dziko lapansi anaona cipulumutso ca Mulungu wathu.
4Pfuulirani kwa Yehova, inu, dziko lonse lapansi;
Kuwitsani ndi kupfuulira mokondwera; inde, yimbirani zomlemekeza.
5Myimbireni Yehova zomlemekeza ndizeze;
Ndi zeze ndi mau a salmo.
6Pfuulani pamaso pa Mfumu Yehova,
Ndi mbetete ndi liu la lipenga,
7Nyanja Ipfuule ndi kudzala kwace;
Dziko lokhalamo anthu ndi iwo okhalamo;
8Mitsinje iombe manja;
Mapiri apfuule pamodzi mokondwera;
9Pamaso pa Yehova, popeza akudza kudzaweruza dziko lapansi;
Adzaweruza dziko lokhalamo anthu ndi cilungamo,
Ndi mitundu ya anthu molunjika,

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 99

Mulungu wamkuru wacifundo alemekezedwe

1Yehova ndiye mfumu; mitundu ya anthu injenjemere;
Iye akhala pakati pa akerubi; dziko lapansi ligwedezeke.
2Yehova ndiye wamkuru m'Ziyoni;
Ndipo akwezeka pamwamba pa mitundu yonse ya anthu.
3Alemekeze dzina lanu lalikuru ndi loopsa;
Ili ndilo loyera.
4Ndipo mphamvu ya mfumu ikonda ciweruzo;
Inu mukhazikitsa zolunjika,
Mucita ciweruzo ndi cilungamo m'Yakobo.
5Mkwezeni Yehova Mulungu wathu,
Ndipo padirani poponderapo mapasa ace:
Iye ndiye Woyera.
6Mwa ansembe ace muli Mose ndi Aroni,
Ndi Samueli mwa iwo akuitanira dzina lace;
Anaitana kwa Yehova, ndipo Iye anawayankha.
7Iye analankhula nao mumtambo woti njo:
Iwo anasunga mboni zace ndi malembawa anawapatsa,
8Munawayankha, Yehova Mulungu wathu:
Munawakhalira Mulungu wakuwakhululukira,
Mungakhale munabwezera cilango pa zocita zao.
9Mkwezeni Yehova Mulungu wathu,
Ndipo gwadirani pa phiri lace loyera;
Pakuti Yehova Mulungu wathu ndiye woyera.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 100

Olengedwa ndi Mulungu amlemekeze

Salmo la Ciyamiko.

1Pfuulirani kwa Yehova, inu, dziko lonse lapansi.
2Tumikirani Yehova ndi cikondwerero:
Idzani pamaso pace ndi kumyimbira mokondwera,
3Dziwani kuti Yehova ndiye Mulungu;
Iyeyu anatilenga, ndipo ife ndife ace;
Ndife anthu ace ndi nkhosa za pabusa pace.
4Lowani ku zipata zace ndi ciyamiko,
Ndi ku mabwalo ace ndi cilemekezo:
Myamikeni; lilemekezeni dzina lace.
5Pakuti Yehova ndiye wabwino; cifundo cace cimamka muyaya;
Ndi cikhulupiriko cace ku mibadwo mibadwo.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 101

Davide akuti adzasamala okhulupirika nadzacotsa oipa

Salmo la Davide.

1Ndidzayimba za cifundo ndi ciweruzo;
Ndidzayimba zakukulemekezani Inu, Yehova.
2Ndidzacita mwanzeru m'njira yangwiro;
Mudzandidzera liti?
Ndidzayenda m'nyumba mwanu ndi mtima wangwiro.
3Sindidzaika cinthu coipa pamaso panga;
Cocita iwo akupatuka padera cindiipira;
Sicidzandimamatira.
4Mtima wopulukira udzandicokera;
Sindidzadziwana naye woipa.
5Wakuneneza mnzace m'tseri ndidzamdula;
Wa maso odzikuza ndi mtima wodzitama sindidzamlola.
6Maso anga ayang'ana okhulupirika m'dziko, kuti akhale ndi Ine;
Iye amene ayenda m'njira yangwiro, iyeyu adzanditumikira Ine.
7Wakucita cinyengo sadzakhala m'kati mwa nyumba yanga;
Wakunena mabodza sadzakhazikika pamaso panga.
8Mamawa onse ndidzadula oipa onse a m'dziko;
Kuduliratu onse akucita zopanda pace ku mudzi wa Yehova.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Wopsinjika apempha Mulungu acitire anthu ace cifundo, amitundu nammverenso

Pemphero la Wozunzika, m'mene anakomoka natsanulira cobnaatira cace pamaso pa Yehova,

1Yehova, imvani pemphero langa,
Ndipo mpfuu wanga ufikire Inu.
2Musandibisire nkhope yanu tsiku la nsautso yanga;
Mundichereze khutu lanu;
Tsiku limene ndiitana ine mundiyankhe msanga,
3Popeza masiku anga akanganuka ngati utsi,
Ndi mafupa anga anyeka ngati nkhuni.
4Mtima wanga ukunga udzu wamweta, nufota;
Popeza ndiiwala kudya mkate wanga.
5Cifukwa ca liu la kubuula kwanga
Mnofu wanga umamatika ku mafupa anga.
6Ndikunga bvuwo m'cipululu;
Ndikhala ngati kadzidzi wa kumabwinja.
7Ndidikira, ndikhala ngati mbawa
Iri yokha pamwamba pa tsindwi.
8Adani anga anditonza tsiku lonse;
Akundiyarukirawo alumbirira ine.
9Pakuti ndadya mapulusa ngati mkate,
Ndi kusanganiza-comwera canga ndi misozi,
10Cifukwa ca ukali wanu ndi kuzaza kwanu;
Popeza munandinyamula ndipo munandigwetsa.
11Masiku anga akunga mthunzi womka m'tali;
Ndipo ine ndauma ngati udzu.
12Koma Inu, Yehova, mukhalabe ku nthawi yonse;
Ndi cikumbukilo canu ku mibadwo mibadwo.
13Inu mudzauka, ndi kucitira nsoni Ziyoni;
Popeza yafika nyengo yakumcitira cifundo, nyengo yoikika.
14Pakuti atumiki anu akondwera nayo miyala yace,
Nacitira cifundo pfumbi lace.
15Pamenepo amitundu adzaopa dzina la Yehova,
Ndi mafumu onse a dziko lapansi ulemerero wanu;
16Pakuti Yehova anamanga Ziyoni,
Anaoneka m'ulemerero wace;
17Anasamalira pemphero la iwo akusowa konse,
Osapepula pemphero lao.
18Ici adzacilembera mbadwo ukudza;
Ndi mtundu wa anthu umene udalengedwa udzamlemekeza Yehova.
19Pakuti anapenya pansi ali kumwamba kuli malo ace opatulika;
Yehova pokhala kumwamba anapenya dziko lapansi;

20Kuti amve kubuula kwa wandende;
Namasule ana a imfa,
21Kuti anthu alalikire dzina la Yehova m'Ziyoni,
Ndi cilemekezo cace m'Yerusalemu;
22Posonkhana pamodzi mitundu ya anthu,
Ndi maufumu kuti atumikire Yehova.
23Iye analanda mphamvu yanga panjira;
Anacepsa masiku anga.
24Ndinati, Mulungu wanga, musandicotse pakati pa masiku anga:
Zaka zanu zikhalira m'mibadwo mibadwo.
25Munakhazika dziko lapansi kalelo;
Ndipo zakumwamba ndizo nchito ya manja anu.
26Zidzatha izi, koma Inu mukhala:
Inde, zidzatha zonse ngati cabvala;
Mudzazisintha ngati maraya, ndipo zidzasinthika:
27Koma Inu ndinu yemweyo,
Ndi zaka zanu sizifikira kutha.
28Ana a atumiki anu adzakhalitsa,
Ndi mbeu zao zidzakhazikika pamaso panu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 103

Alemekeze Yehovapa cifundo cace cacikuru

Salmo la Da vide.

1Lemekeza Yehova, moyo wanga;
Ndi zonse za m'kati mwanga zilemekeze dzina lace loyera.
2Lemekeza Yehova, moyo wanga,
Ndi kusaiwala zokoma zace zonse aticitirazi:
3Amene akhululukira mphulupulu zako zonse;
Naciritsa nthenda zako zonse;
4Amene aombola moyo wako ungaonongeke;
Nakubveka korona wa cifundo ndi nsoni zokoma:
5Amene akhutitsa m'kamwa mwako ndi zabwino;
Nabweza ubwana wako unge mphungu.
6Yehova acitira onse osautsidwa Cilungamo ndi ciweruzo.
7Analangiza Mose njira zace,
Ndi ana a Israyeli macitidwe ace.
8Yehova ndiye wa nsoni zokoma ndi wacisomo,
Wosakwiya msanga, ndi wa cifundo cocuruka.
9Sadzatsutsana nao nthawi zanse;
Ndipo sadzasunga mkwiyo wace kosatha.
10Sanaticitira monga mwa zolakwa zathu,
Kapena kutibwezera monga mwa mphulupulu zathu.
11Pakuti monga m'mwamba mutalikira ndi dziko lapansi,
Motero cifundo cace cikulira iwo akumuopa Iye.
12Monga kum'mawa kutanimpha ndi kumadzulo,
Momwemo anatisiyanitsira kutali zolakwa zathu.
13Monga atate acitira ana ace cifundo,
Yehova acitira cifundo iwo akumuopa Iye.
14Popeza adziwa mapangidwe athu;
Akumbukila kuti ife ndife pfumbi.
15Koma munthu, masiku ace akunga udzu;
Aphuka monga duwa la kuthengo.
16Pakuti mphepo ikapitapo pakhala palibe:
Ndi malo ace salidziwanso.
17Koma cifundo ca Yehova ndico coyambira nthawi yosayamba
kufikira nthawi yosatha kwa iwo akumuopa Iye,
Ndi cilungamo cace kufikira kwa ana a ana;
18Kwa iwo akusunga cipangano cace,
Ndi kwa iwo akukumbukila malangizo ace kuwacita.
19Yehova anakhazika mpando wacifumu wace Kumwamba;
Ndi ufumu wace ucita mphamvu ponsepo,
20Lemekezani Yehova, inu angelo ace;
A mphamvu zolimba, akucita mau ace,
Akumvera liu la mau ace.

21Lemekezani Yehova, inu makamu ace onse;
Inu atumiki ace akucita comkondweretsa Iye,
22Lemekezani Yehova, inu, nchito zace zonse,
Ponse ponse pali ufumu wace:
Lemekeza Yehova, moyo wanga iwe.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 104

Ulemerero wa Mulungu m'zolengedwa ndi m'kuzisunga komwe

1Lemekeza Yehova, moyo wanga;
Yehova, Mulungu wanga, Inu ndinu wamkurukuru;
2Mubvala ulemu ndi cifumu.
Amene mudzikuta nako kuunika monga ndi cobvala;
Ndi kuyala thambo ngati nsaru yocinga;
3Amene alumikiza mitanda ya zipinda zace m'madzi;
Naika makongwa akhale agareta ace;
Nayenda pa mapiko a mphepo;
4Amene ayesa mphepo amithenga ace;
Lawi la moto atumiki ace;
5Anakhazika dziko lapansi pa maziko ace,
Silidzagwedezeka ku nthawi yonse.
6Mudalikuta ndi nyanja ngati ndi cobvala;
Madzi anafikira pamwamba pa mapiri,
7Pa kudzudzula kwanu anathawa;
Anathawa msanga liu la bingu lanu;
8Anakwera m'mapiri, anatsikira m'zigwa,
Kufikira malo mudawakonzeratu.
9Munaika malire kuti asapitirireko;
Kuti asabwererenso kuphimba dziko lapansi.
10Atumiza akasupe alowe m'makwawa;
Ayenda pakati pa mapiri:
11Zimamwamo nyama zonse za kuthengo;
Mbidzi zipherako ludzu lao.
12Mbalame za mlengalenga zifatsa pamenepo,
Zimayimba pakati pa mitawi.
13Iye amwetsa mapiri mocokera m'zipinda zace:
Dziko lakhuta zipatso za nchito zanu.
14Ameretsa msipu ziudye ng'ombe,
Ndi zitsamba acite nazo munthu;
Naturutse cakudya cocokera m'nthaka;
15Ndi vinyo wokondweretsa mtima wa munthu,
Ndi mafuta akunyezimiritsa nkhope yace,
Ndi mkate wakulimbitsa mtima wa munthu.
16Mitengo ya Mulungu yadzala ndi madzi;
Mikungudza ya ku Lebano imene anaioka;
17M'mwemo mbalame zimanga zisa zao;
Pokhala cumba mpa mitengo ya mikungudza,
18Mapiri atali ndiwo ayenera zinkhoma;
Pamatanthwe mpothawirapo mbira.
19Anaika mwezi nyengo zace;
Dzuwa lidziwa polowera pace.
20Muika mdima ndipo pali usiku;
Pamenepo zituruka zirombo zonse za m'thengo.
21Misona ya mkango ibangula potsata nyama yao,
Nifuna cakudya cao kwa Mulungu.
22Poturuka dzuwa, zithawa, Zigona pansi m'ngaka mwao.
23Pamenepo munthu aturukira ku nchito yace,
Nagwiritsa kufikira madzulo.
24Nchito zanu zicurukadi, Yehova!

Munazicita zonse mwanzeru;
Dziko lapansi lidzala naco cuma canu.
25Nyanja siyo, yaikuru ndi yacitando,
M'mwemo muli zokwawa zosawerengeka;
Zamoyo zazing'ono ndi zazikuru.
26M'mwemo muyenda zombo;
Ndi livyatanu amene munamlenga aseweremo.
27Izi zonse zikulindirirani,
Muzipatse cakudya cao pa nyengo yace.
28Cimene muzipatsa zigwira;
Mufumbatula dzanja lanu, zikhuta zabwino.
29Mukabisa nkhope yanu, ziopsedwa;
Mukalanda mpweya wao, zikufa,
Nizibwerera kupfumbi kwao.
30Potumizira mzimu wanu, zilengedwa;
Ndipo mukonzanso nkhope ya dziko lapansi.
31Ulemerero wa Yehova ukhale kosatha;
Yehova akondwere mu nchito zace;
32Amene apenyerera pa dziko lapansi, ndipo linjenjemera;
Akhudza mapiri, ndipo afuka.
33Ndidzayimbira Yehova m'moyo mwanga:
Ndidzayimbira Mulungu wanga zomlemekeza pokhala ndiripo.
34Pomlingirira Iye pandikonde;
Ndidzakondwera mwa Yehova.
35Ocimwa athedwe ku dziko lapansi,
Ndi oipa asakhalenso.
Yamika Yehova, moyo wanga.
Haleluya.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 105

Alemekeza Yehova pa zodabwiza adazicitira ana a Israyeli

1Yamikani Yehova, itanirani pa dzina lace;
Bukitsani mwa mitundu ya anthu zocita Iye.
2Myimbireni, myimbireni zomlemekeza;
Fotokozerani zodabwiza zace zonse.
3Mudzitamandire ndi dzina lace loyera:
Mitima yao ya iwo ofunsira Yehova ikondwere.
4Funani Yehova, ndi mphamvu yace;
Funsirani nkhope yace nthawi zonse.
5Kumbukilani zodabwiza zace adazicita;
Zizindikilo zace ndi maweruzo a pakamwa pace;
6Inu mbeu za Abrahamu, mtumiki wace,
Inu ana a Yakobo, osankhika ace.
7Iye ndiye Yehova, Mulungu wathu;
Maweruzo ace akhala pa dziko lonse lapansi.
8Akumbukila cipangano cace kosatha,
Mauwo anawalamulira mibadwo zikwi;
9Cipanganoco anapangana ndi Abrahamu,
Ndi lumbiro lace ndi Isake;
10Ndipo anaciimikira Yakobo, cikhale malemba,
Cikhale cipangano cosatha kwa Israyeli.
11Ndi kunena kuti, Ndidzakupatsa iwe dziko la Kanani,
Gawo la colandira cako;
12Pokhala iwo anthu owerengeka,
Inde, anthu pang'ono, ndi alendo m'mwemo;
13Nayendayenda kucokera mtundu wina kufikira mtundu wina,
Kucokera ufumu wina kufikira anthu ena.
14Sanalola munthu awasautse;
Ndipo anadzudzula mafumu cifukwa ca iwowa;
15Ndi kuti musamakhudza odzozedwa anga,
Musamacitira coipa aneneri anga.
16Ndipo anaitana njala igwere dziko;
Anatyola mcirikizo wonse wa mkate.
17Anawatsogozeratu munthu;
Anamgulitsa Yosefe akhale kapolo:
18Anapweteka miyendo yace ndi matangadza;
Anamgoneka m'unyolo;
19Kufikira nyengo yakucitika maneno ace;
Mau a Yehova anamuyesa.
20Mfumuyo anatuma munthu nammasula;
Woweruza mitundu ya anthu anamtsegulira.
21Anamuika akhale woyang'anira nyumba yace,
Ndi woweruza wa pa zace zonse:

22Amange nduna zace iye mwini,
Alangize akulu ace adziwe nzeru. 23Pamenepo Israyeli analowa m'Aigupto;
Ndi Yakobo anakhala mlendo m'dziko la Hamu.
24Ndipo anacurukitsatu mtundu wa anthu ace,
Nawapatsa mphamvu yoposa owasautsa.
25Anasanduliza mitima yao, kuti adane nao anthu ace,
Kuti acite monyenga ndi atumiki ace.
26Anatuma Mose mtumiki wace, Ndi Aroni amene adamsankha.
27Anaika pakati pao zizindikilo zace,
Ndi zodabwiza m'dziko la Hamu.
28Anatumiza mdima ndipo kunada;
Ndipo sanapikisana nao mau ace.
29Anasanduliza madzi ao akhale mwazi,
Naphanso nsomba zao.
30Dziko lao linacuruka acule,
M'zipinda zomwe za mafumu ao.
31Ananena, ndipo inadza mitambo ya nchenche,
Ndi nsabwe kufikira m'malire ao onse.
32Anawapatsa mvula yamatalala,
Lawi la moto m'dziko lao.
33Ndipo anapanda mipesa yao, ndi mikuyu yao;
Natyola mitengo kufikira m'malire ao onse.
34Ananena, ndipo linadza dzombe
Ndi mphuci, ndizo zosawerengeka,
35Ndipo zinadya zitsamba zonse za m'dziko mwao,
Zinadyanso zipatso za m'nthaka mwao.
36Ndipo Iye anapha acisamba onse m'dziko mwao
Coyambira ca mphamvu yao yonse.
37Ndipo anawaturutsa pamodzi ndi siliva ndi golidi:
Ndi mwa mafuko ao munalibe mmodzi wokhumudwa.
38Aigupto anakondwera pakucoka iwo;
Popeza kuopsa kwao kudawagwera.
39Anayala mtambo uwaphimbe;
Ndi moto uunikire usiku,
40Anafunsa ndipo Iye anadzetsa zinziri.
Nawakhuritsa mkate wakumwamba.
41Anatsegula pathanthwe, anaturukamo madzi;
Nayenda pouma ngati mtsinje.
42Popeza anakumbukila mau ace oyera,
Ndi Abrahamu mtumiki wace.
43Potero anaturutsa anthu ace ndi kusekerera,
Osankhika ace ndi kupfuula mokondwera.
44Ndipo anawapatsa maiko a amitundu;

Iwo ndipo analanda zipatso za nchito ya anthu:
45Kuti asamalire malemba ace,
Nasunge malamulo ace.
Haleluya.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Israyeli anapikisana ndi Yehova kwambiri, Iye nawalanga nawalanditsanso Amlemekezepo

1Haleluya.
Yamikani Yehova; pakuti Iye ndiye wabwino:
Pakuti cifundo cace ncosatha.
2Adzafotokoza ndani nchito zamphamvu za Yehova,
Adzamveketsa ndani cilemekezo cace conse?
3Odala iwo amene asunga ciweruzo,
Iye amene acita cilungamo nthawi zonse.
4Mundikumbukile, Yehova, monga momwe mubvomerezana ndi anthu anu;
Mundionetsa cipulumutso canu:
5Kuti ndione cokomaco ca osankhika anu,
Kuti ndikondwere naco cikondwerero ca anthu anu,
Kuti ndidzitamandire pamodzi ndi colowa canu.
6Talakwa pamodzi ndi makolo athu;
Tacita mphulupulu, tacita coipa.
7Makolo athu sanadziwitsa zodabwiza zanu m'Aigupto;
Sanakumbukila zacifundo zanu zaunyinji;
Koma anapikisana ndi Inu kunyanja, ku Nyanja Yofiira.
8Koma anawapulumutsa cifukwa ca dzina lace,
Kuti adziwitse cimphamvu cace.
9Ndipo anadzudzula Nyanja Yofiira, niiphwa:
Potero anawayendetsa mozama ngati m'cipululu.
10Ndipo anawapulumutsa m'dzanja la iye amene anawada,
Nawaombola ku dzanja la mdani.
11Ndipo madziwo anamiza owasautsa;
Sanatsala mmodzi yense.
12Pamenepo anabvomereza mau ace;
Anayimbira comlemekeza.
13Koma anaiwala nchito zace msanga;
Sanalindira uphungu wace:
14Popeza analaka-lakatu kucidikhako,
Nayesa Mulungu m'cipululu.
15Ndipo anawapatsa copempha iwo;
Koma anaondetsa mitima yao.
16Ndipo kumisasa anacita nao nsanje Mose
Ndi Aroni woyerayo wa Yehova.
17Dziko lidayasama nilidameza Datani,
Ndipo linafotsera gulu la Abiramu.
18Ndipo m'gulu mwao mudayaka moto;
Lawi lace lidapsereza oipawo.
19Anapanga mwana wa ng'ombe ku Horebu,

Nagwadira fano loyenga.
20M'mwemo anasintha ulemerero wao
Ndi fanizo la ng'ombe Yakudya msipu.
21Anaiwala Mulungu mpulumutsi wao,
Amene anacita zazikulu m'Aigupto;
22Zodabwiza m'dziko la Hamu,
Zoopsa ku Nyanja Yofiira.
23Potero Iye adati awaononge,
Pakadapanda Mose wosankhika wace, kuima pamaso pace pagamukapo,
Kubweza ukali wace ungawaononge,
24Anapeputsanso dziko lofunika,
Osabvomereza mau ace;
25Koma anadandaula m'mahema mwao,
Osamvera mau a Yehova.
26Potero anawasamulira dzanja lace,
Kuti awagwetse m'cipululu:
27Kugwetsanso mbeu zao mwa amitundu,
Ndi kuwabalalitsa m'maiko maiko.
28Ndipo anadzipatikiza ndi BaalaPeori,
Nadyanso nsembe za akufa.
29Ndipo anamkwiyitsa nazo zocita zao;
Kotero kuti mliri unawagwera.
30Pamenepo panauka Pinehasi, nacita cilango:
Ndi mliriwo unaletseka.
31Ndipo adamuyesa iye wacilungamo,
Ku mibadwo mibadwo ku nthawi zonse.
32Anautsanso mkwiyo wace ku madzi a Meriba,
Ndipo kudaipira Mose cifukwa ca iwowa:
33Pakuti anawawitsa mzimu wace,
Ndipo analankhula zosayenera ndi milomo yace.
34Sanaononga mitunduyo ya anthu,
Imene Mulungu adawauza;
35Koma anasokonekerana nao amitundu,
Naphunzira nchito zao:
36Ndipo anatumikira mafano ao,
Amene anawakhalira msampha:
37Ndipo anapereka ana ao amuna ndi akazi nsembe ya kwa ziwanda,
38Nakhetsa mwazi wosacimwa, ndi wo mwazi wa ana ao amuna ndi akazi,
Amene anawaperekera nsembe mafano a Kanani;
M'mwemo analidetsa dziko ndi mwaziwo.
39Ndipo anadziipsa nazo nchito zao,

Nacita cigolololo nao macitidwe ao.
40Potero udayaka mkwiyo wa Yehova pa anthu ace,
Nanyansidwa Iye ndi colowa cace.
41Ndipo anawapereka m'manja a amitundu;
Ndipo odana nao anacita ufumu pa iwo.
42Adani ao anawasautsanso,
Nawagonjetsa agwire mwendo wao.
43Iye anawalanditsa kawiri kawiri;
Koma anapikisana ndi Iye mwa uphungu wao,
Ndi mphulupulu zao zinawafoketsa,
44Koma anapenya nsautso yao,
Pakumva kupfuula kwao:
45Ndipo anawakumbukila cipangano cace,
Naleza monga mwa kucuruka kwa cifundo cace.
46Ndipo anawacitira kuti apeze nsoni
Pamaso pa onse amene adawamanga ndende.
47Tipulumutseni, Yehova, Mulungu wathu,
Ndi kutisokolotsa kwa amitundu,
Kuti tiyamike dzina lanu loyera,
Ndi kudzitamandira naco cilemekezo canu.
48Wodala Yehova, Mulungu wa Israyeli,
Kuyambira kosayamba kufikira kosatha.
Ndi anthu onse anene, Amen.
Haleluya,

©The Bible Society of Malawi, 1992

Olanditsidwa, alendo, omangidwa, odwala, amarinyero ndi onse ena alemekeze Yehova

1Yamikani Yehova pakuti Iye ndiye wabwino;
Pakuti cifundo cace ncosatha.
2Atere oomboledwa a Yehova,
Amene anawaombola m'dzanja la wosautsa;
3Nawasokolotsa kumaiko,
Kucokera kum'mawa ndi kumadzulo,
Kumpoto ndi kunyanja.
4Anasokera m'cipululu, m'njira yopanda anthu;
Osapeza mudzi wokhalamo.
5Anamva njala ndi ludzu,
Moyo wao unakomoka m'kati mwao.
6Pamenepo anapfuulira kwa Yehova mumsauko mwao,
Ndipo anawalanditsa m'kupsinjika kwao.
7Ndipo anawatsogolera pa njira yolunjika,
Kuti amuke ku mudzi wokhalamo.
8Ayamike Yehova cifukwa ca cifundo cace,
Ndi zodabwiza zace za kwa ana a anthu!
9Pakuti akhutitsa mtima wolakalaka,
Nadzaza mtima wanjala ndi zabwino.
10Iwo akukhala mumdima ndi mu mthunzi wa imfa,
Omangika ndi kuzunzika ndi citsulo;
11Popeza anapikisana nao mau a Mulungu,
Napeputsa uphungu wa Wam'mwambamwamba;
12Kotero kuti anagonjetsa mtima wao ndi cobvuta;
Iwowa anakhumudwa koma panalibe mthandizi.
13Pamenepo anapfuulira kwa Yehova mumsauko mwao,
Ndipo anawapulumutsa m'kupsinjika kwao.
14Anawaturutsa mumdima ndi mu mthunzi wa imfa,
Nadula zomangira zao.
15Ayamike Yehova cifukwa ca cifundo cace,
Ndi zodabwiza zace za kwa ana a anthu!
16Popeza adaswa zitseko zamkuwa,
Natyola mipiringidzo yacitsulo.
17Anthu opusa azunzika cifukwa ca zolakwa zao,
Ndi cifukwa ca mphulupulu zao.
18Mtima wao unyansidwa naco cakudya ciri conse;
Ndipo ayandikira zipata za imfa.
19Pamenepo apfuulira kwa Yehova m'kusauka kwao,
Ndipo awapulumutsa m'kupsinjika kwao.
20Atumiza mau ace nawaciritsa,
Nawapulumutsa ku cionongeko cao.

21Ayamike Yehova cifukwa ca cifundo cace,
Ndi zodabwiza zace za kwa ana a anthu!
22Ndipo apereke nsembe zaciyamiko,
Nafotokozere nchito zace ndi kupfuula mokondwera.
23Iwo akutsikira kunyanja nalowa m'zombo,
Akucita nchito zao pa madzi akuru;
24Iwowa apenya nchito za Yehova,
Ndi zodabwiza zace m'madzi ozama.
25Popeza anena, nautsa namondwe,
Amene autsa mafunde ace.
26Akwera kuthambo, atsikira kozama;
Mtima wao usungunuka naco coipaco.
27Adzandira napambanitsa miyendo ngati munthu woledzeta,
Nathedwa nzeru konse.
28Pamenepo apfuulira kwa Yehova m'kusauka kwao,
Ndipo awaturutsa m'kupsinjika kwao.
29Asanduliza namondwe akhale bata,
Kotero kuti mafunde ace atonthole.
30Pamenepo akondwera, popeza pagwabata;
Ndipo Iye awatsogolera kudooko afumko.
31Ayamike Yehova cifukwa ca cifundo cace,
Ndi zodabwiza zace za kwa ana a anthu!
32Amkwezenso mu msonkhano wa anthu,
Namlemekeze pokhala akulu.
33Asanduliza mitsinje ikhale cipululu,
Ndi akasupe a madzi akhale nthaka youma;
34Dziko lazipatso, likhale lakhulo,
Cifukwa ca coipa ca iwo okhalamo.
35Asanduliza cipululu cikhale tha wale,
Ndi dziko louma likhale akasupe a madzi.
36Ndi apo akhalitsa anjala,
Kuti amangeko mudzi wokhalamo anthu;
37Nafese m'minda, naoke mipesa,
Ndiyo vakubata zipatso zolemeza.
38Ndipo awadalitsa, kotero kuti, acuruka kwambiri;
Osacepsanso zoweta zao.
39Koma acepanso, nawerama,
Cifukwa ca cisautso, coipa ndi cisoni.
40Atsanulira cimpepulo pa akulu,
Nawasokeretsa m'cipululu mopanda njira.
41Koma aika waumphawi pamsanje posazunzika,
Nampatsa mabanja ngati gulu la nkhosa.
42Oongoka mtima adzaciona nadzasekera;
Koma cosalungama conse citseka pakamwa pace.

43Wokhala nazo nzeru asamalire izi,
Ndipo azindikire zacifundo za Yehova,

©The Bible Society of Malawi, 1992

Davide ayimbira Mulungu womgonjetsera adani

Nyimbo. Salmo la Davide.

1Wakhazikika mtima wanga, Mulungu;
Ndidzayimba, inde ndidzayimba zolemekeza, ndiko ulemerero wanga.
2Galamukani, cisakasa ndi zeze;
Ndidzauka ndekha mamawa.
3Ndidzakuyamikani mwa mitundu ya anthu, Yehova:
Ndipo ndidzayimba zakukulemekezani mwa anthu.
4Pakuti cifundo canu ncacikuru kupitirira kumwamba,
Ndi coonadi canu kufikira mitambo.
5Kwezekani pamwamba pa thambo, Mulungu;
Ndi ulemerero wanu pamwamba pa dziko lonse lapansi.
6Kuti okondedwa anu alanditsidwe,
Pulumutsani ndi dzanja lanu lamanja ndipo mutibvomereze.
7Mulungu analankhula m'ciyero cace; ndidzakondwerera:
Ndidzagawa Sekemu; ndidzayesa muyeso cigwa ca Sukoti.
8Gileadi ndi wanga: Manase ndi wanga;
Ndi Efraimu ndiye mphamvu ya mutu wanga;
Yuda ndiye wolamulira wanga.
9Moabu ndiye mkhate wanga;
Pa Edomu ndidzaponya nsapato yanga;
Ndidzapfuulira Filistiya,
10Adzandifikitsa ndani m'mudzi wa m'linga?
Adzanditsogolera ndani ku Edomu?
11Si ndinu Mulungu, amene mwatitaya
Osaturuka nao magulu athu?
12Tithandizeni mumsauko;
Pakuti cipulumutso ca munthu ndi cabe.
13Mwa Mulungu tidzacita molimbika mtima:
Ndipo Iye adzapondereza otisautsa.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 109

Davide apempha Mulungu alange oipa, amlanditse m'manja mwao

Kwa Mkulu wa Nyimbo; Salmo la Davide,

1Mulungu wa cilemekezo canga, musakhale cete;
2Pakuti pakamwa pa woipa ndi pakamwa pa cinyengo
pananditsegukira;
Anandilankhulira ndi m'kamwa mwa bodza.
3Ndipo anandizinga ndi mau a udani,
Nalimbana nane kopanda cifukwa.
4M'malo mwa cikondi canga andibwezera udani;
Koma ine, kupemphera ndiko.
5Ndipo anandisenza coipa m'malo mwa cokoma,
Ndi udani m'malo mwa cikondi canga.
6Muike munthu woipa akhale mkuru wace;
Ndi mdani aime pa dzanja lamanja lace.
7Ponenedwa mlandu wace aturuke wotsutsika;
Ndi pemphero lace likhale ngati kucimwa.
8Masiku ace akhale owerengeka;
Wina alandire udindo wace.
9Ana ace akhale amasiye, Ndi mkazi wace wamasiye.
10Ana ace akhale amcirakuyenda ndi opemphapempha;
Afunefune zosowa zao kucokera m'mabwinja mwao.
11Wokongoletsa agwire zonse ali nazo;
Ndi alendo alande za nchito yace.
12Pasakhale munthu wakumdtira cifundo;
Kapena kucitira cokoma ana ace amasiye.
13Zidzukulu zace zidulidwe;
Dzina lao lifafanizidwe mu mbadwo ukudza.
14Mphulupulu za makolo ace zikumbukike ndi Yehova;
Ndi cimo la mai wace lisafafanizidwe.
15Zikhale pamaso pa Yehova cikhalire,
Kuti adule cikumbukilo cao kucicotsera ku dziko lapansi.
16Cifukwa kuti sanakumbukila kucita cifundo,
Koma analondola wozunzika ndi waumphawi,
Ndi wosweka mtima, kuti awaphe.
17Inde, anakonda kutemberera, ndipo kudamdzera mwini;
Sanakondwera nako kudalitsa, ndipo kudamkhalira kutali.
18Anabvalanso temberero ngati maraya,
Ndipo lidamlowa m'kati mwace ngati madzi,
Ndi ngati mafuta m'mafupa ace.
19Limkhalire ngati cobvala adzikuta naco,
Ndi lamba limene adzimangirira nalo m'cuuno cimangirire,
20Ici cikhale mphotho ya otsutsana nane yowapatsa Yehova,

Ndi ya iwo akunenera coipa moyo wanga.
21Koma Inu, Yehova Ambuye, mucite nane cifukwa ca dzina lanu;
Ndilanditseni popeza cifundo canu ndi cabwino.
22Pakuti ine ndine wozunzika ndi waumphawi,
Ndi mtima wanga walaswa m'kati mwanga.
23Ndamuka ngati mthunzi womka m'tali
Ndiingidwa kwina ndi kwina ngati dzombe.
24Mabondo anga agwedezeka cifukwa ca kusala;
Ndi mnofu wanga waonda posowa mafuta.
25Ndiwakhaliranso cotonza;
Pakundiona apukusa mutu.
26Ndithandizeni Yehova, Mulungu wanga:
Ndipulumutseni monga mwa cifundo canu;
27Kuti adziwe kuti ici ndi dzanja lanu;
Kuti Inu Yehova munacicita.
28Atemberere iwowa, koma mudalitse ndinu;
Pakuuka iwowa adzacita manyazi, koma mtumiki wanu
adzakondwera.
29Otsutsana nane abvale manyazi,
Nadzikute naco cisokonezo cao ngati ndi copfunda.
30Ndidzayamika Yehova kwakukuru pakamwa panga;
Ndi pakati pa anthu aunyinji ndidzamlemekeza.
31Popeza adzaima pa dzanja lamanja la waumphawi
Kumpulumutsa kwa iwo akuweruza koipa moyo wace.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Ufumu wa Ambuye

Salmo la Davide,

1Yehova ananena kwa Ambuye wanga, Khalani pa dzanja lamanja
langa,
Kufikira nditaika adani anu copondapo mapazi anu.
2Yehova adzatumiza ndodo ya mphamvu yanu kucokera ku Ziyoni;
Citani ufumu pakati pa adani anu.
3Anthu anu adzadzipereka eni ace tsiku la camuna canu:
M'moyera mokometsetsa, mobadwira tnatanda kuca,
Muli nae mame a ubwana wanu.
4Yehova walamulira, ndipo sadzasintha,
Inu ndinu wansembe kosatha
Monga mwa cilongosoko ca Melikizedeke.
5Yehova pa dzanja lamanja lako
Adzaphwanya mafumu tsiku la mkwiyo wace.
6Adzaweruza mwa amitundu,
Adzadzaza dziko ndi mitembo;
Adzaphwanya mitu m'maiko ambiri.
7Adzamwa ku mtsinje wa panjira;
Cifukwa cace adzaweramutsa mutu wace.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 111

Alemekeza Mulungu pa nchito zao zazikuru zokoma

1Haleluya.
Ndidzayamika Yehova ndi mtima wonse,
Mu upo wa oongoka mtima, ndi mumsonkhano.
2Nchito za Yehova nzazikuru,
Zofunika ndi onse akukondwera nazo.
3Cocita Iye nca ulemu, ndi ukuru:
Ndi cilungamo cace cikhalitsa kosatha.
4Anacita cokumbukitsa zodabwiza zace;
Yehova ndiye wa cisomo ndi nsoni zokoma.
5Anapatsa akumuopa Iye cakudya;
Adzakumbukila cipangano cace kosatha.
6Anaonetsera anthu ace mphamvu ya nchito zace,
Pakuwapatsa colowa ca amitundu.
7Nchito za manja ace ndizo caonadi ndi ciweruzo;
Malangizo ace onse ndiwo okhulupirika.
8Acirikizika ku nthawi za nthawi,
Acitika m'coonadi ndi cilunjiko,
9Anatumizira anthu ace cipulumutso;
Analamulira cipangano cace kosatha;
Dzina lace ndilo loyera ndi loopedwa.
10Kumuopa Yehova ndiko ciyambi ca nzeru;
Onse akucita cotero ali naco cidziwitso cokoma;
Cilemekezo cace cikhalitsa kosatha.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 112

Adalitsidwa akuopa Mulungu

1Haleluya.
Wodala munthu wakuopa Yehova,
Wakukondwera kwambiri ndi malamulo ace,
2Mbeu yace idzakhala yamphamvu pa dziko lapansi;
Mbadwo wa oongoka mtima udzadalitsidwa.
3M'nyumba mwace mudzakhala akatundu ndi cuma:
Ndi cilungamo cace cikhala cikhalire.
4Kuupika kuturukira oongoka mtima mumdima;
Iye ndiye wacisomo; ndi wansoni ndi wolungama.
5Wodala munthu wakudtira cifundo, nakongoletsa;
Adzalimbika nao mlandu wace poweruzidwa.
6Popeza sadzagwedezeka nthawi zonse:
Wolunguna adzakumbukika ku nthawi yosatha.
7Sadzaopa mbiri yoipa;
Mtima wace ngwokhazikika, wakhulupirira Yehova.
8Mtima wace ngwocirikizika, sadzacita mantha,
Kufikira ataona cofuna iye pa iwo omsautsa.
9Anagawagawa, anapatsa aumphawi;
Cilungamo cace cikhalitsa kosatha;
Nyanga yace idzakwezeka ndi ulemu.
10Woipa adzaziona, nadzapsa mtima;
Adzakukuta mano, nadzasungunuka;
Cokhumba oipa cidzatayika.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 113

Anthu onse alemekeze dzina la Mulungu wothandiza aumphawi

1Haleluya;
Lemekezani, inu atumiki a Yehova;
Lemekezani dzina la Yehova,
2Lodala dzina la Yehova.
Kuyambira tsopano kufikira kosatha.
3Citurukire dzuwa kufikira kulowa kwace
Lilemekezedwe dzina la Yehova.
4Yehova akwezeka pamwamba pa amitundu onse,
Ulemerero wace pamwambamwamba.
5Akunga Yehova Mulungu wathu ndani?
Amene akhala pamwamba patali,
6Nadzicepetsa apenye
Zam'mwamba ndi za pa dziko lapansi.
7Amene autsa wosauka lrumcotsa kupfumbi,
Nakweza waumphawi kumcotsa kudzala.
8Kuti amkhalitse pamodzi ndi akulu,
Pamodzi ndi akulu a anthu ace.
9Asungitsa nyumba mkazi wosaonamwana,
Akhale mai wokondwera ndi ana.
Haleluya.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 114

Alemekeze Mulungu pa cipulumutso cija ca m'Aigupto

1M'mene Israyeli anaturuka ku Aigupto,
Nyumba ya Yakobo kwa anthu a cinenedwe cacilendo;
2Yuda anakhala malo ace oyera, Israyeli ufumu wace.
3Nyanjayo inaona, nithawa;
Yordano anabwerera m'mbuyo.
4Mapiri anatumphatumpha ngati nkhosa zamphongo,
Timapiri ngati ana a nkhosa.
5Unathawanji nawe, nyanja iwe?
Unabwerereranji m'mbuyo, Yordano iwe?
6Munatumpha-tumphiranji ngati nkhosa zamphongo, mapiri inu?
Ngati ana a nkhosa, zitunda inu?
7Unjenjemere, dziko lapansi iwe, pamaso pa Ambuye,
Pamaso pa Mulungu wa Yakobo;
8Amene anasanduliza thanthwe likhale thawale lamadzi,
Nsangalabwi ikhale kasupe wamadzi.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 115

Mulungu ndi wa ulemerero, mafano ndiwo acale

1Kwa ife ai, Yehova, kwa ife ai, Koma kwa dzina lanu patsani ulemerero,
Cifukwa ca cifundo canu, ndi coonadi canu.
2Aneneranji amitundu,
Ali kuti Mulungu wao?
3Koma Mulungu wathu ndiye ali m'mwamba;
Acita ciri conse cimkonda.
4Mafano ao ndiwo a siliva ndi golidi,
Nchito za manja a anthu.
5Pakamwa ali napo, koma osalankhula;
Maso ali nao, koma osapenya;
6Makutu ali nao, koma osamva;
Mphuno ali nazo, koma osanunkhiza;
7Manja ali nao, koma osagwira;
Mapazi ali nao, koma osayenda;
Kapena sanena pammero pao,
8Adzafanana nao iwo akuwapanga;
Ndi onse akuwakhulupirira,
9Israyeli, khulupirira Yehova:
Ndiye mthandizi wao ndi cikopa cao.
10Nyumba ya Aroni, khulupirira Yehova:
Ndiye mthandizi wao, ndi cikopa cao.
11Inu akuopa Yehova, khulupirirani Yehova;
Ndiye mthandizi wao ndi cikopa cao.
12Yehova watikumbukila; adzatidalitsa:
Adzadalitsa nyumba ya Israyeli;
Adzadalitsa nyumba ya Aroni.
13Adzadalitsa iwo akuopa Yehova,
Ang'ono ndi akuru.
14Yehova akuonjezereni dalitso, Inu ndi ana anu.
15Odalitsika inu a kwa Yehova,
Wakulenga kumwamba ndi dziko lapansi.
16Kunena za kumwamba, kumwamba ndiko kwa Yehova;
Koma dziko lapansi analipereka kwa ana a anthu.
17Akufa salemekeza Yehova,
Kapena ali yense wakutsikira kuli cete:
18Koma ife tidzalemekeza Yehova
Kuyambira tsopano kufikira nthawi yonse.
Haleluya.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 116

Cikondi ndi ciyamiko ca pa Mulungu cifukwa ca cipalumutso cace

1Ndimkonda, popeza Yehova amamva,
Mau anga ndi kupemba kwanga.
2Popeza amandicherera khutu lace,
Cifukwa cace ndidzaitanira Iye masiku anga onse.
3Zingwe za imfa zinandizinga,
Ndi zowawa za manda zinandigwira:
Ndinapeza nsautso ndi cisoni.
4Pamenepo ndinaitana dzina la Yehova;
Ndikuti, Yehova ndikupemphani landitsani moyo wanga.
5Yehova ngwa cifundo ndi wolungama;
Ndi Mulungu wathu ngwa nsoni.
6Yehova asunga opusa;
Ndidafoka ine, koma anandipulumutsa,
7Ubwere moyo wanga ku mpumulo wako;
Pakuti Yehova anakucitira cokoma.
8Pakuti munalanditsa moyo wanga kuimfa,
Maso anga kumisozi, Mapazi anga, ndingagwe.
9Ndidzayenda pamaso pa Yehova M'dziko la amoyo.
10Ndinakhulupirira, cifukwa cace ndinalankhula;
Ndinazunzika kwambiri.
11Pofulumizidwa mtima ndinati ine,
Anthu Onse nga mabodza.
12Ndidzabwezera Yehova ciani
Cifukwa ca zokoma zace zonse anandicitira?
13Ndidzanyamula cikho ca cipulumutso,
Ndipo ndidzaitanira dzina la Yehova,
14Ndidzacitazowindazanga za kwa Yehova,
Tsopano, pamaso pa anthu ace onse.
15Imfa ya okondedwa ace
Nja mtengo wace pamaso pa Yehova.
16Ndiloleni, Yehova, indetu ndine mtumiki wanu;
Ndine mtumiki wanu, mwana wa mdzakazi wanu;
Mwandimasulira zondimanga,
17Ndidzapereka kwa Inu nsembe yaciyamiko,
Ndipo ndidzaitanira dzina la Yehova.
18Ndidzacita zowinda zanga za kwa Yehova,
Tsopano, pamaso pa anthu ace onse;
19M'mabwalo a nyumba ya Yehova,
Pakati pa inu, Yerusalemu. Haleluya.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 117

Alemekezedwe Mulungu pa cifundo cace

1Lemekezani Yehova, amitundu onse;
Myimbireni, anthu onse.
2Pakuti cifundo cace ca pa ife ndi cacikuru;
Ndi coonadi ca Yehova ncosatha.
Haleluya.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 118

Wa Salmo alemekeza Mulungu womlanditsa m'manja mwa adani

1Yamikani Yehova; pakuti Iye ndiye wabwino;
Pakuti cifundo cace ncosatha.
2Anene tsono Israyeli,
Kuti cifundo cace ncosatha.
3Anene tsono nyumba ya Aroni,
Kuti cifundo cace ncosatha.
4Anene tsono iwo akuopa Yehova,
Kuti cifundo cace ncosatha.
5M'mene ndinasautsika ndinaitanira pa Yehova;
Anandiyankha Dandiika motakasuka Yehova.
6Yehova ndi wanga; sindidzaopa;
Adzandicitanji munthu?
7Yehova ndi wanga, mwa iwo akundithandiza;
M'mwemo ndidzaona cofuna ine pa iwo akundida,
8Kuthawira kwa Yehova nkokoma
Koposa kukhulupirira munthu.
9Kuthawira kwa Yehova nkokoma
Koposa kukhulupirira akulu,
10Amitundu onse adandizinga,
Zedi, m'dzina la Yehova ndidzawaduladula.
11Adandizinga, inde, adandizinga:
Indedi, m'dzinala Yehova ndidzawaduladula.
12Adandizinga ngati njuci;
Anazima ngati moto waminga;
Indedi, m'dzina la Yehova ndidzawaduladula.
13Kundikankha anandikankha ndikadagwa;
Koma Yehova anandithandiza.
14Yehova ndiye mphamvu yanga ndi nyimbo yanga;
Ndipo anakhala cipulumutso canga.
15M'mahema a olungama muli liu lakupfuula mokondwera ndi la cipulumutso:
16Dzanja lamanja la Yehova licita mwamphamvu.
17Sindidzafa koma ndidzakhala ndi moyo,
Ndipo ndidzafotokozera nchito za Yehova.
18Kulanga anandilangadi Yehova:
Koma sanandipereka kuimfa ai.
19Nditsegulireni zipata za cilungamo;
Ndidzalowamo, ndidzayamika Yehova.
20Cipata ca Yehova ndi ici;
Olungama adzalowamo.
21Ndidzakuyamikani, popeza munandiyankha,

Ndipo munakhala cipulumutso canga,
22Mwala umene omangawo anaukana
Wakhala mutu wa pangondya.
23Ici cidzera kwa Yehova;
Ncodabwiza ici pamaso pathu.
24Tsiku ili ndilo adaliika Yehova;
Tidzasekera ndi kukondwera m'mwemo.
25Tikupemphani, Yehova, tipulumutseni tsopano;
Tikupemphani, Yehova, tipindulitseni tsopano.
26Wodala wakudzayo m'dzina la Yehova;
Takudalitsani kocokera m'nyumba ya Yehova.
27Yehova ndiye Mulungu, amene anatiunikira;
Mangani nsembe ndi zingwe, ku nyanga za guwa la nsembe.
28Inu ndinu Mulungu wanga, ndipo ndidzakuyamikani;
Ndinu Mulungu wanga, ndidzakukwezani.
29Yamikani Yehova, pakuti Iye ndiye wabwino,
Pakuti cifundo cace ncosatha.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Cilamulo ca Mulungu ndi cokometsetsa. Adalitsidwa akucisunga

1Odala angwiro m'mayendedwe ao,
Akuyenda m'cilamulo ca Yehova.
2Odala iwo akusunga mboni zace,
Akumfuna ndi mtima wonse;
3Inde, sacita cosalungama;
Ayenda m'njira zace.
4Inu munatilamulira.
Tisamalire malangizo anu ndi cangu,
5Ha! mwenzi zitakhazikika njira zanga
Kuti ndisamalire malemba anu.
6Pamenepo sindidzacita manyazi,
Pakupenyerera malamulo anu onse.
7Ndidzakuyanrikani ndi mtima woongoka,
Pakuphunzira maweruzo anu olungama.
8Ndidzasamalira malemba anu:
Musandisiye ndithu.
9Mnyamata adzayeretsa mayendedwe ace bwanji?
Akawasamalira monga mwa mau anu.
10Ndinakufunani ndi mtima wanga wonse;
Ndisasokere kusiyana nao malamulo anu.
11Ndinawabisa mau anu mumtima mwanga,
Kuti ndisalakwire Inu.
12Inu ndinu wodala Yehova;
Ndiphunzitseni malemba anu.
13Ndinafotokozera ndi milomo yanga
Maweruzo onse a pakamwa panu,
14Ndinakondwera m'njira ya mboni zanu,
Koposa ndi cuma conse,
15Ndidzalingirira pa malangizo anu,
Ndi kupenyerera mayendedwe anu.
16Ndidzadzikondweretsa nao malemba anu;
Sindidzaiwala mau anu,
17Mucitire cokoma mtumiki wanu kuti ndikhale ndi moyo;
Ndipo ndidzasamalira mau anu.
18Munditsegulire maso, kuti ndipenye
Zodabwiza za m'cilamulo canu.
19Ine ndine mlendo pa dziko lapansi;
Musandibisire malamulo anu.
20Mtima wanga wasweka ndi kukhumba
Maweruzo anu nyengo zonse.
21Munadzudzula odzikuza otembereredwa,

Iwo akusokera kusiyana nao malamulo anu.
22Mundicotsere cotonza, ndi cimpepulo;
Pakuti ndinasunga mboni zanu.
23Nduna zomwe zinakhala zondineneza;
Koma mtumiki wanu analingirira malemba anu.
24Mboni zanu zomwe ndizo zondikondwetsa,
Ndizo zondipangira nzeru.
25Moyo wanga umamatika ndi pfumbi;
Mundipatse moyo monga mwa mau anu.
26Ndinafotokozera njira zanga, ndipo munandiyankha:
Mundiphunzitse malemba anu.
27Mundizindikiritse njira ya malangizo anu;
Kuti ndilingalire zodabwiza zanu.
28Moyo wanga wasungunuka ndi cisoni:
Mundilimbitse monga mwa mau anu.
29Mundicotsere njira ya cinyengo;
Nimundipatse mwacifundo cilamulo canu.
30Ndinasankha njira yokhulupirika;
Ndinaika maweruzo anu pamaso, panga,
31Ndimamatika nazo mboni zanu;
Musandicititse manyazi, Yehova.
32Ndidzathamangira njira ya malamulo anu,
Mutakulitsa mtima wanga.
33Mundiphunzitse, Yehova, njira ya malemba anu;
Ndidzaisunga kufikira kutha kwace.
34Mundizindikiritse, ndipo ndidzasunga malamulo anu;
Ndidzawasamalira ndi mtima wanga wonse.
35Mundiyendetse mopita malamulo anu;
Pakuti ndikondwera m'menemo.
36Lingitsani mtima wanga ku mboni zanu,
Si ku cisiriro ai.
37Mucititse mlubza maso anga ndisapenye zacabe,
Mundipatse moyo mu njira yanu.
38Limbitsirani mtumiki wanu mau anu,
Ndiye wodzipereka kukuopani.
39Mundipatutsire cotonza canga ndiciopaco;
Popeza maweruzo anu ndi okoma.
40Taonani, ndinalira malangizo anu;
Mundipatse moyo mwa cilungamo canu.
41Ndipo cifundo canu cindidzere, Yehova,
Ndi cipulumutso canu, monga mwa mau anu.
42Kuti ndikhale nao mau akuyankha wonditonza;
Popeza ndikhulupirira mau anu.
43Ndipo musandicotsere ndithu mau a coonadi pakamwa panga;

Pakuti ndinayembekeza maweruzo anu.
44Potero ndidzasamalira malamulo anu cisamalire
Ku nthawi za nthawi.
45Ndipo ndidzayenda mwaufulu;
Popeza ndinafuna malangizo anu.
46Ndidzalankhulanso za umboni wanu pamaso pa mafumu,
Osacitapo manyazi.
47Ndipo ndidzadzikondweretsa nao malamulo anu,
Amene ndiwakonda.
48Ndidzakwezanso manja anga ku malamulo anu, amene ndiwakonda;
Ndipo ndidzalingalira pa malemba anu.
49Kumbukilani mau a kwa mtumiki wanu,
Amene munandiyembekezetsa nao.
50Citonthozo canga m'kuzunzika kwanga ndi ici;
Pakuti mau anu anandipatsa moyo.
51Odzikuza anandinyoza kwambiri:
Koma sindinapatukanso naco cilamulo canu.
52Ndinakumbukila maweruzo anu kuyambira kale, Yehova,
Ndipo ndinadzitonthoza.
53Ndinasumwa kwakukuru,
Cifukwa ca oipa akusiya cilamulo canu.
54Malemba anu anakhala nyimbo zanga
M'nyumba ya ulendo wanga,
55Usiku ndinakumbukila dzina lanu, Yehova,
Ndipo ndinasamalira cilamulo canu.
56Ici ndinali naco,
Popeza ndinasunga malangizo anu.
57Yehova ndiye gawo langa:
Ndinati ndidzasunga mau anu.
58Ndinapemba pankhope panu ndi mtima wanga wonse:
Mundicitire cifundo monga mwa mau anu.
59Ndinaganizira njira zanga,
Ndipo ndinabweza mapazi anga atsate mboni zanu.
60Ndinafulumira, osacedwa,
Kusamalira malamulo anu.
61Anandikulunga nazo zingwe za oipa;
Koma sindinaiwala cilamulo canu.
62Pakati pa usiku ndidzauka kukuyamikani
Cifukwa ca maweruzo anu olungama.
63Ine ndine wakuyanjana nao onse akukuopani,
Ndi iwo akusamalira malangizo anu.
64Dziko lapansi lidzala naco cifundo canu, Yehova;
Mundiphunzitse malemba anu.

65Munacitira mtumiki wanu cokoma, Yehova,
Monga mwa mau anu.
66Mundiphunzitse cisiyanitso ndi nzeru;
Pakuti ndinakhulupirira malamulo anu.
67Ndisanazunzidwe ndinasokera; Koma tsopano ndisamalira mau anu.
68Inu ndinu wabwino, ndi wakucita zabwino;
Mundiphunzitse malemba anu.
69Odzikuza anandipangira bodza:
Ndidzasunga malangizo anu ndi mtima wanga wonse.
70Mtima wao unona ngati mafuta;
Koma ine ndikondwera naco cilamulo canu.
71Kundikomera kuti ndinazunzidwa;
Kuti ndiphunzire malemba anu.
72Cilamulo ca pakamwa panu cindikomera
Koposa golidi ndi siliva zikwi zikwi.
73Manja anu anandilenga nandiumba;
Mundizindikiritse, kuti ndiphunzire malemba anu.
74Iwo amene akuopani adzandiona ine nadzakondwera;
Popeza ndayembekezera mau anu;
75Ndidziwa kuti maweruzo anu ndiwo olungama, Yehova,
Ndi kuti munandizunza ine mokhulupirika.
76Cifundo canu cikhaletu cakunditonthoza, ndikupemphani,
Monga mwa mau anu kwa mtumiki wanu.
77Nsoni zokoma zanu zindidzere, kuti ndikhale ndi moyo;
Popeza cilamulo canu cindikondweretsa.
78Odzikuza acite manyazi, popeza anandicitira monyenga ndi bodza:
Koma ine ndidzalingalira malangizo anu.
79Iwo akuopa Inu abwere kwa ine,
Ndipo adzadziwa mboni zanu.
80Mtima wanga ukhale wangwiro m'malemba anu;
Kuti ndisacite manyazi.
81Moyo wanga unakomoka ndi kukhumba cipulumutso canu:
Ndinayembekezera mau anu.
82Maso anga anatha mphamvu ndi kukhumba mau anu,
Ndikuti, Mudzanditonthoza liti?
83Popeza ndakhala ngati thumba lofukirira;
Koma sindiiwala malemba anu.
84Masiku a mtumiki wanu ndiwo angati?
Mudzaweruza liti iwo akundilondola koipa?
85Odzikuza anandikumbira mbuna,
Ndiwo osasamalira cilamulo canu.
86Malamulo anu onse ngokhulupirika;

Andilondola nalo bodza; ndithandizeni.
87Akadandithera pa dziko lapansi; Koma ine sindinasiya malangizo anu.
88Mundipatse moyo monga mwa cifundo canu;
Ndipo ndidzasamalira mboni ya pakamwa panu,
89Mau anu aikika kumwamba,
Kosatha, Yehova.
90Cikhulupiriko canu cifikira mibadwo mibadwo;
Munakhazikitsa dziko lapansi, ndipo likhalitsa.
91Kunena za maweruzo anu alimbikira kufikira lero;
Pakuti onsewa ndiwo atumiki anu.
92Cilamulo canu cikadapanda kukhala cikondweretso canga,
Ndikadatayika m'kuzunzika kwanga.
93Sindidzaiwala malangizo anu nthawi zonse;
Popeza munandipatsa nao moyo.
94Ine ndine wanu, ndipulumutseni
Pakuti ndinafuna malangizo anu.
95Oipa anandilalira kundiononga;
Koma ndizindikira mboni zanu.
96Ndinapenya malekezero ace a ungwiro wonse;
Koma lamulo lanu ndi lotakasuka ndithu.
97Ha! Ndikondadi cilamulo canu;
Ndilingiriramo ine tsiku lonse.
98Malamulo anu andipatsa nzeru yakuposa adani anga;
Pakuti akhala nane cikhalire.
99Ndiri nayo nzeru yakuposa aphunzitsi anga onse;
Pakuti ndilingalira mboni zanu.
100Ndizindikira koposa okalamba
Popeza ndinasunga malangizo anu.
101Ndinaletsa mapazi anga njira iri yonse yoipa,
Kuti ndisamalire mau anu.
102Sindinapatukana nao maweruzo anu;
Pakuti Inu munandiphunzitsa.
103Mau anu azunadi powalawa ine!
Koposa uci m'kamwa mwanga.
104Malangizo anu andizindikiritsa;
Cifukwa cace ndidana nao mayendedwe onse acinyengo,
105Mau anu ndiwo nyali ya ku mapazi anga,
Ndi kuunika kwa panjira panga,
106Ndinalumbira, ndipo ndinatsimikiza mtima,
Kuti ndidzasamalira maweruzo anu olungama.
107Ndazunzika kwambiri:
Ndipatseni moyo, Yehova, monga mwa mau anu.
108Landirani, Yehova, zopereka zaufulu za pakamwa panga,

Ndipo ndiphunzitseni maweruzo anu.
109Moyo wanga ukhala m'dzanja langa cikhalire;
Koma sindiiwala cilamulo canu.
110Oipa anandichera msampha;
Koma sindinasokera m'malangizo anu.
111Ndinalandira mboni zanu zikhale colandira cosatha;
Pakuti ndizo zokondweretsa mtima wanga.
112Ndinalingitsa mtima wanga ucite malemba anu,
Kosatha, kufikira cimatiziro.
113Ndidana nao a mitima iwiri;
Koma ndikonda cilamulo canu.
114Inu ndinu pobisalapo panga, ndi cikopa canga;
Ndiyembekezera mau anu.
115Mundicokere ocita zoipa inu;
Kuti ndisunge malamulo a Mulungu wanga.
116Mundicirikize monga mwa mau anu, kuti ndikhale ndi moyo;
Ndipo ndisacite manyazi pa ciyembekezo canga.
117Mundigwirizize ndipo ndidzapulumutsidwa,
Ndipo ndidzasamalira malemba anu cisamalire.
118Mupepulaonseakusokeram'malemba anu;
Popeza cinyengo cao ndi bodza.
119Mucotsa oipa onse a pa dziko lapansi ngati mphala:
Cifukwa cace ndikonda mboni zanu.
120Thupi langa linjenjemera ndi kuopa Inu;
Ndipo ndicita mantha nao maweruzo anu.
121Ndinacita ciweruzo ndi cilungamo;
Musandisiyira akundisautsa.
122Mumkhalire cikole mtumiki wanucimkomere;
Odzikuza asandisautse.
123Maso anga anatha mphamvu pafuna cipulumutso canu,
Ndi mau a cilungamo canu.
124Mucitire mtumiki wanu monga mwa cifundo canu,
Ndipo ndiphunzitseni malemba anu,
125Ine ndine mtumiki wanu, ndizindikiritseni;
Kuti ndidziwe mboni zanu.
126Yafika nyengo yakuti Yehova acite kanthu;
Pakuti anaswa cilamulo canu.
127Cifukwa cace ndikonda malamulo anu
Koposa golidi, Inde golidi woyengeka,
128Cifukwa cace ndiyesa ngolunjika malangizo anu onse akunena zonse;
Koma ndidana nazo njira zonse zonyenga.
129Mboni zanu nzodabwiza; Cifukwa cace moyo wanga uzisunga,
130Potsegulira mau anu paunikira;

Kuzindikiritsa opusa.
131Ndinatsegula pakamwa panga, ndi kupuma wefu wefu;
Popeza ndinakhumba malamulo anu.
132Munditembenukire, ndi kundicitira cifundo,
Monga mumatero nao akukonda dzina lanu.
133Kfiazikitsanimapaziangam'mau anu;
Ndipo zisandigonjetse zopanda pace ziri zonse.
134Mundiombole ku nsautso ya munthu:
Ndipo ndidzasamalira malangizo anu.
135Muwalitse nkhope yanu pa mtumiki wanu;
Ndipo mundiphunzitse malemba anu.
136Maso anga atsitsa mitsinje ya madzi,
Popeza sasamalira cilamulo canu.
137Inu ndinu wolungama, Yehova,
Ndipo maweruzo anu ndiwo olunjika.
138Mboni zanuzo mudazilamulira
Ziri zolungama ndi zokhulupirika ndithu.
139Cangu canga cinandithera,
Popeza akundisautsa anaiwala mau anu.
140Mau anu ngoyera ndithu;
Ndi mtumiki wanu awakonda.
141Wamng'ono ine, ndi wopepulidwa;
Koma sindiiwala malemba anu.
142Cilungamo canu ndico cilungamo cosatha;
Ndi cilamulo canu ndico coonadi.
143Kusautsika ndi kupsinjika kwandigwera;
Koma malamulo anu ndiwo ondikondweretsa ine.
144Mboni zanu ndizo zolungama kosatha;
Mundizindikiritse izi, ndipo ndidzakhala ndi moyo.
145Ndinaitana ndi mtima wanga wonse; mundiyankhe, Yehova;
Ndidzasunga malemba anu.
146Ndinaitanira Inu; ndipulumutseni,
Ndipo ndidzasamalira mboni zanu.
147Ndinapfuula kusanace:
Ndinayembekezera mau anu.
148Maso anga anakumika malonda a usiku,
Kuti ndilingirire mau anu.
149Imvani liu langa monga mwa cifundo canu;
Mundipatse moyo monga mwa kuweruza kwanu, Yehova.
150Otsata zaciwembu andiyandikira;
Akhala kutali ndi cilamulo canu.
151Inu muli pafupi, Yehova;
Ndipo malamulo anu onse ndiwo coonadi,
152Kuyambira kale ndinadziwa mu mboni zanu,

Kuti munazikhazika kosatha,
153Penyani kuzunzika kwanga, nimundilanditse;
Pakuti sindiiwala cilamulo canu.
154Mundinenere mlandu wanga, nimundiombole;
Mundipatse moyo monga mwa mau anu.
155Cipulumutso citalikira oipa;
Popeza safuna malemba anu.
156Zacifundo zanu ndi zazikuru, Yehova;
Mundipatse moyo monga mwa maweruzo anu.
157Ondilondola ndi ondisautsa ndiwoambiri;
Koma sindinapatukana nazo mboni zanu.
158Ndinapenya ocita monyenga, ndipo ndinanyansidwa nao;
Popeza sasamalira mau anu.
159Penyani kuti ndikonda malangizo anu;
Mundipatse moyo, Yehova, monga mwa cifundo canu.
160Ciwerengero ca mau anu ndico coonadi;
Ndi maweruzo anu olungama onse akhala kosatha.
161Nduna zinandilondola kopanda cifukwa;
Koma mtima wanga ucita mantha nao mau anu.
162Ndikondwera nao mau anu,
Ngati munthu wakupeza zofunkha zambiri.
163Ndidana nalo bodza ndi kunyansidwa nalo;
Koma ndikonda cilamulo canu.
164Ndikulemekezani kasanu ndi kawiri, tsiku limodzi,
Cifukwa ca maweruzo anu alungama.
165Akukonda cilamulo canu ali nao mtendere wambiri;
Ndipo alibe cokhumudwitsa.
166Ndinayembekeza cipulumutso canu, Yehova,
Ndipo ndinacita malamulo anu.
167Moyo wanga unasamalira mboni zanu;
Ndipo ndizikonda kwambiri.
168Ndinasamalira malangizo anu ndi mboni zanu;
Popeza njira zanga zonse ziri pamaso panu,
169Kupfuula kwanga kuyandikire pamaso pano, Yehova;
Mundizindikiritse monga mwa mau anu.
170Kupemba kwanga kudze pamaso panu;
Mundilanditse monga mwa mau anu.
171Milomo yanga iturutse cilemekezo;
Popeza mundiphunzitsa malemba anu.
172Lilime langa liyimbire mau anu;
Pakuti malamulo anu onse ndiwo olungama.
173Dzanja lanu likhale lakundithandiza
Popezandinasankha malangizo anu.
174Ndinakhumba cipulumutso canu, Yehova;

Ndipo cilamulo canu ndico condikondweretsa.
175Mzimu wanga ukhale ndi moyo, ndipo udzakulemekezani;
Ndipo maweruzo anu andithandize.
176Ndinasocera ngati nkhosa yotayika; funani mtumiki wanu;
Pakuti sindiiwala malamulo anu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 120

Apempha Mulungu amlanditse pa Omnamiza

Nyimbo yokwerera.

1Ndinapfuulira kwa Yehova mu msauko wanga,
Ndipo anandibvomereza,
2Yehova, landitsani moyo wanga ku milomo ya mabodza,
Ndi ku lilime lonyenga.
3Adzakuninkhanji, adzakuonjezeranji,
Lilime lonyenga iwe?
4Mibvi yakuthwa ya ciphona.
Ndi makara tsanya.
5Tsoka ine, kuti ndiri mlendo m'Meseke,
Kuti ndigonera m'mahema a Kedara!
6Moyo wanga unakhalitsa nthawi
Pamodzi ndi iye wakudana nao mtendere.
7Ine ndikuti, Mtendere;
Koma polankhula ine, iwowa akuti, Nkhondo.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo121

Mulungu Msungi wokhulupirika wa anthu ace

Nyimbo yokwerera.

1Ndikweza maso anga kumapiri:
Thandizo langa lidzera kuti?
2Thandizo langa lidzera kwa Yehova,
Wakulenga zakumwamba ndi dziko lapansi.
3Sadzalola phazi lako literereke:
Iye amene akusunga sadzaodzera.
4Taonani, wakusunga Israyea
Sadzaodzera kapena kugona.
5Yehova ndiye wakukusunga;
Yehova ndiye mthunzi wako wa ku dzanja lako lamanja.
6Dzuwa silidzawamba usana,
Mwezi sudzakupanda usiku.
7Yehova adzakusunga kukucotsera zoipa ziri zonse;
Adzasunga moyo wako.
8Yehova adzasungira kuturuka kwako ndi kulowa kwako,
Kuyambira tsopano kufikira nthawi zonse.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 122

Apempherera mtendere wa Yerusalemu

Nyimbo yokwerera: ya Davide.

1Ndinakondwera m'mene ananena nane,
Tiyeni ku nyumba ya Yehova.
2Mapazi athu alinkuima M'zipata zanu, Yerusalemu.
3Yerusalemu anamangidwa
Ngati mudzi woundana bwino:
4Kumene akwerako mafuko, ndiwo mafuko a Yehova;
Akhale mboni ya kwa Israyeli,
Ayamike dzina la Yehova.
5Pakuti pamenepo anaika mipando ya ciweruzo,
Mipando ya nyumba ya Davide.
6Mupempherere mtendere wa Yerusalemu;
Akukonda inu adzaona phindu.
7M'linga mwako mukhale mtendere,
M'nyumba za mafumu mukhale phindu.
8Cifukwa ca abale anga ndi mabwenzi anga,
Ndidzanena tsopano, Mukhale mtendere mwa inu.
9Cifukwa ca nyumba ya Yehova Mulungu wathu
Ndidzakufunira zokoma,

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 123

Pemphero la wonyozedwa

Nyimbo yokwerera.

1Ndikweza maso anga kwa Inu,
Kwa Inu wakukhala kumwamba.
2Taonani, monga maso a anyamata ayang'anira dzanja la ambuye ao,
Monga maso a adzakazi ayang'anira dzanja la mbuye wao wamkazi:
Momwemo maso athu ayang'anira Yehova Mulungu wathu,
Kufikira aticitira cifundo.
3Muticitire cifundo, Yehova, muticitire cifundo;
Pakuti takhuta kwambiri ndi mnyozo.
4Moyo wathu wakhuta ndithu
Ndi kuseka kwa iwo osasowa kanthu,
Ndi mnyozo wa odzikuza.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 124

Mulungu yekha walanditsa anthu ace

Nyimbo vokwerera: ya Davide,

1Akadapanda kukhala nafe Yehova,
Anene tsono Israyeli;
2Akadapanda kukhala nafe Yehova,
Pakutiukira anthu:
3Akadatimeza amoyo,
Potipsera mtima wao.
4Akadatimiza madziwo,
Mtsinje ukadapita pa moyo wathu;
5Madzi odzikuza akadapita pa moyo wathu.
6Alemekezedwe Yehova,
Amene sanatipereka kumano kwao tikhale cakudya cao.
7Moyo wathu unaonjoka ngati mbalame mu msampha wa msodzi;
Msampha unatyoka ndi ife tinaonioka.
8Thandizo lathu liri m'dzina la Yehova,
Wolenga kumwamba ndi dziko lapansi.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 125

Okhulupirira Yehova akhazikika mtima

Nyimbo yokwerera.

1Iwo akukhulupirira Yehova
Akunga phiri la Ziyoni, losasunthika, likhazikika kosatha,
2Monga mapiri azinga Yerusalemu,
Momwemo Yehova azinga anthu ace,
Kuyambira tsopano kufikira nthawi zonse.
3Pakuti ndodo yacifumu ya coipa siidzapumula pa gawo la olungama;
Kuti olungama asaturutse dzanja lao kucita cosalungama,
4Citirani cokoma, Yehova, iwo okhala okoma;
Iwo okhala oongoka mumtima mwao.
5Koma iwo akupatuka kutsata njira zao zokhotakhota,
Yehova adzawacotsa pamodzi ndi ocita zopanda pace.
Mtendere ukhale pa Israyeli.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 126

Ayamikira mokondwerera kuti Mulungu anabweza ukapolo wao

Nyimbo yokwerera.

1Pobweza Yehova ukapolo wa Ziyoni,
Tinakhala ngati anthu akulota.
2Pamenepo pakamwa pathu panadzala ndi kuseka,
Ndi lilime lathu linapfuula mokondwera;
Pamenepo anati mwa amitundu,
Yehova anawacitira iwo zazikuru,
3Yehova anaticitira ife zazikuru;
Potero tikhala okondwera.
4Bwezani ukapolo wathu, Yehova,
Ngati mitsinje ya ku Mwera.
5Akubzala ndi misozi adzatuta ndi kupfuula mokondwera.
6Iye amene ayendayenda nalira, ponyamula mbeu yakufesa;
Adzabweranso ndithu ndi kupfuula mokondwera, alikunyamula mitolo yace.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Madalitso onse, a m'banja omwe, acokera kwa Mulungu

Nyimbo vokwerera; ya Solomo.

1Akapanda kumanga nyumba Yehova,
Akuimanga agwiritsa nchito cabe;
Akapanda kusunga mudzi Yehoya,
Mlonda adikira cabe.
2Kuli cabe kwa inu Rulawirira mamawa ndi kusagonerapo madzulo,
Kudya mkate wosautsa kuupeza;
Kuli tero kuti izi apatsa okondedwa ace ngati m'tulo.
3Taonani ana ndiwo colandira ca kwa Yehova;
Cipatso ca m'mimba ndico mphotho yace.
4Ana a ubwana wace wa munthu
Akunga mibvi m'dzanja lace la ciphona.
5Wodala munthu amene anadzaza nayo phodo lace:
Sadzacita manyazi iwo,
Pakulankhula nao adani kucipata.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 128

Wakuopa Yehova adalitsidwa m'banja mwace

Nyimbo yokwerera.

1Wodala yense wakuopa Yehova, Wakuyenda m'njira zace.
2Pakuti udzadya za nchito ya manja ako;
Wodala iwe, ndipo kudzakukomera.
3Mkazi wako adzanga mpesa wopatsa m'mbali za nyumba yako;
Ana ako adzanga timitengo ta azitona pozinga podyera pako.
4Taonani, m'mwemo adzadalitsika
Munthu wakuopa Yehova.
5Yehova adzakudalitsa ali m'Ziyoni
Ndipo udzaona zokoma za Yerusalemu masiku onse a moyo wako.
6Inde, udzaona zidzukulu zako.
Mtendere ukhale ndi Israyeli.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 129

Israyeli asautsidwa koma osafafanizidwa

Nyimbo yokwerera.

1Anandisautsa kawiri kawiri kuyambira ubwana wanga,
Anene tsono Israyeli;
2Anandisautsa kawiri kawiri kuyambira ubwana wanga;
Koma sanandilaka.
3Olima analima pamsana panga;
Anatalikitsa mipere yao.
4Yehova ndiye wolungama;
Anadulatu zingwe za oipa.
5Acite manyazi nabwerere m'mbuyo.
Onse akudana naye Ziyoni.
6Akhale ngati udzu womera patsindwi,
Wakufota asanauzule;
7Umene womweta sadzaza nao dzanja lace,
Kapena womanga mitolo sakupatira manja.
8Angakhale opitirirapo sanena,
Dalitso la Mulungu likhale pa inu;
Tikudalitsani m'dzina la Yehova.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 130

Pemphero lakuti akhululukidwe

Nyimbo yokwerera.

1M'mozamamo ndinakupfuulirani, Yehova.
2Ambuye, imvani liu langa;
Makutu anu akhale cimverere
Mau a kupemba kwanga.
3Mukasunga mphulupulu, Yehova,
Adzakhala ciriri ndani, Ambuye?
4Koma kwa Inu kuli cikhululukiro,
Kuti akuopeni.
5Ndilindira Yehova, moyo wanga ulindira,
Ndiyembekeza mau ace.
6Moyo wanga uyang'anira Ambuye,
Koposa alonda matanda kuca;
Inde koposa alonda matanda kuca.
7Israyeli, uyembekezere Yehova;
Cifukwa kwa Yehova kuli cifundo,
Kwaonso kucurukira ciombolo.
8Ndipo adzaombola Israyeli
Ku mphulupulu zace zonse.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 131

Kudzicepetsa kwa Davide pakupemphera

Nyimbo yokwerera, ya Davide.

1Yehova, mtima wanga sunadzikuza
Ndi maso anga sanakwezeka;
Ndipo sindinatsata zazikuru,
Kapena zodabwiza zondiposa.
2Indedi, ndinalinganiza ndi kutontholetsa moyo wanga;
Ngati mwana womletsa kuyamwa amace,
Moyo wanga ndiri nao ngati mwana womletsa kuyamwa.
3Israyeli, uyembekezere Yehova,
Kuyambira tsopano kufikira kosatha.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 132

Davide asamalira kacisi ndi likasa. Lonjezano la Mulungu

Nyimbo yokwerera.

1Yehova, kumbukilani Davide Kuzunzika kwace konse;
2Kuti analumbira Yehova,
Nawindira Wamphamvuyo wa Yakobo, ndi kuti,
3Ngati ndidzalowa pakhomo pa nyumba yanga,
Ngati ndidzakwera pa kama logonapo;
4Ngati ndidzalola maso anga agone,
Kapena zikope zanga ziodzere;
5Kufikira nditapezera Yehova malo,
Cokhalamo Wamphamvuyo wa Yakobo?
6Taonani, tinacimva m'Efrata;
Tinacipeza ku cidikha ca kunkhalango.
7Tidzalowa mokhalamo Iye;
Tidzagwadira ku mpando wa mapazi ace.
8Ukani, Yehova, lowani ku mpumulo wanu;
Inu ndi hema wa mphamvu yanu,
9Ansembe anu abvale cilungamo;
Ndi okondedwa anu apfuule mokondwera.
10Cifukwa ca Davide mtumiki wanu
Musabweze nkhope ya wodzozedwa wanu.
11Yehova analumbira Davide zoona;
Sadzalibweza; ndi kuti,
Wa iwo okhala zipatso za thupi lako ndidzaika pa mpando wacifumu wako.
12Ana ako akasunga cipangano canga
Ndi mboni yanga imene ndidzawaphunzitsa,
Ana aonso adzakhala pa mpando wanu ku nthawi zonse,
13Pakuti Yehova anasankha Ziyoni;
Analikhumba likhale pokhala pace; ndi kuti,
14Pampumulo panga mpano posatha:
Pano ndidzakhala; pakuti ndakhumbapo.
15Ndidzadalitsatu cakudya cace;
Aumphawi ace ndidzawakhutitsa ndi mkate.
16Ndipo ansembe ace ndidzawabveka ndi cipulumutso:
Ndi okondedwa ace adzapfuulitsa mokondwera.
17Apo ndidzaphukitsira Davide nyanga;
Ndak onzeraru wodzozedwa wanga nyali.
18Ndidzawabvekaadani ace ndi manyazi
Koma pa iyeyu korona wace adzambveka.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 133

Cikondano ca abale ndi cokoma

Nyimbo yokwerera; ya Davide.

1Onani, nkokoma ndi kokondweretsa ndithu
Kuti abale akhale pamodzi!
2Ndiko ngati mafuta a mtengo wace pamutu,
Akutsikira ku ndebvu,
Inde ku ndebvu za Aroni;
Akutsikira ku mkawo wa zobvala zace
3Ngati mame a ku Hermoni,
Akutsikira pa mapiri a Ziyoni:
Pakuti pamenepo Yehova analamulira dalitsolo,
Ndilo moyo womka muyaya,

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 134

Afulumizidwa anthu kulemekeza Yehova

Nyimbo vokwerera,

1Taonani, lemekezani Yehova, atumiki a Yehova inu nonse,
Akuimirira m'nyumba ya Yehova usiku,
2Kwezani manja anu ku malo oyera,
Nimulemekeze Yehova.
3Yehova, ali m'Ziyoni, akudalitseni;
Ndiye amene analenga kumwamba ndi dziko lapansi.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 135

Mulungu alemekezedwa pa ukulu wace. Mafano ndi acabe

1Haleluya;
Lemekezani dzina la Yehova;
Lemekezani inu atumiki a Yehova:
2Inu akuimirira m'nyumba ya Yehova,
M'mabwalo a nyumba ya Mulungu wathu.
3Lemekezani Yehova; pakuti Yehova ndiye wabwino;
Muyimbire zolemekeza dzina lace; pakuti nkokondweretsa kutero.
4Pakuti Yehova anadzisankhira Yakobo,
Israyeli, akhale cuma cace ceni ceni.
5Pakuti ndidziwa kuti Yehova ndi wamkuru,
Ndi Ambuye wathu aposa milungu yonse.
6Ciri conse cimkonda Yehova acicita,
Kumwamba ndi pa dziko lapansi, m'nyanja ndi mozama monse.
7Akweza mitambo icokere ku malekezero a dziko lapansi;
Ang'animitsa mphezi zidzetse mvula;
Aturutsa mphepo mosungira mwace.
8Anapanda oyamba a Aigupto,
Kuyambira munthu kufikira zoweta.
9Anatumiza zizindikilo ndi zodabwiza pakati pako,
Aigupto iwe, Pa Farao ndi pa omtumikira onse.
10Ndiye amene anapanda amitundu ambiri.
Napha mafumu amphamvu;
11Sihoni mfumu ya Aamori,
Ndi Ogi mfumu ya Basana,
Ndi maufumu onse a Kanani:
12Ndipo anapereka dziko lao likhale cosiyira,
Cosiyira ca kwa Israyeli anthu ace.
13Dzina lanu, Yehova, likhala kosatha;
Cikumbukilo canu, Yehova, kufikira mibadwo mibadwo.
14Pakuti Yehova adzaweruza anthu ace,
Koma adzaleka atumiki ace.
15Mafano a amitundu ndiwo siliva ndi golidi,
Nchito ya manja a anthu.
16Pakamwa ali napo koma osalankhula;
Maso ali nao, koma osapenya;
17Makutu ali nao, koma osamva;
Inde, pakamwa pao palibe mpweya.
18Akuwapanga adzafanana nao;
Inde, onse akuwakhulupirira.
19A nyumba ya Israyeli inu, lemekezani Yehova:
A nyumba ya Aroni inu, lemekezani Yehova:
20A nyumba ya Levi inu, lemekezani Yehova:

Inu akuopa Yehova, lemekezani Yehova.
21Alemekezedwe Yehova kucokera m'Ziyoni,
Amene akhala m'Yerusalemu.
Haleluya,

©The Bible Society of Malawi, 1992

Mulungu alemekezedwe pa cifundo cace

1Yamikani Yehova pakuti ndiye wabwino:
Pakuti cifundo cace ncosatha.
2Yamikani Mulungu wa milungu:
Pakuti cifundo cace ncosatha.
3Yamikani Mbuye wa ambuye:
Pakuti cifundo cace ncosatha.
4Amene yekha acita zodabwiza zazikuru:
Pakuti cifundo cace ncosatha.
5Amene analenga zakumwamba mwanzeru:
Pakuti cifundo cace ncosatha.
6Amene anayala dziko lapansi pamwamba pa madzi:
Pakuti cifundo cace ncosatha.
7Amene analenga miuni yaikuru:
Pakuti cifundo cace ncosatha.
8Dzuwa liweruze usana:
Pakuti cifundo cace ncosatha.
9Mwezi ndi nyenyezi ziweruze usiku;
Pakuti cifundo cace ncosatha.
10Iye amene anapandira Aaigupto ana ao oyamba:
Pakuti cifundo cace ncosatha.
11Naturutsa Israyeli pakati pao;
Pakuti cifundo cace ncosatha.
12Ndi dzanja lamphamvu, ndi mkono wotambasuka:
Pakuti cifundo cace ncosatha.
13Amene anagawa magawo Nyanja Yofiira:
Pakuti cifundo cace ncosatha.
14Napititsa Israyeli pakati pace;
Pakuti cifundo cace ncosatha.
15Nakhutula Farao ndi khamu lace m'Nyanja Yofiira:
Pakuti cifundo cace ncosatha.
16Amene anatsogolera anthu ace m'cipululu:
Pakuti cifundo cace ncosatha.
17Amene anapanda mafumu akulu:
Pakuti cifundo cace ncosatha,
18Ndipo anawapha mafumu omveka:
Pakuti cifundo cace ncosatha.
19Sihoni mfumu ya Aamori;
Pakuti cifundo cace ncosatha.
20Ndi ogi mfumu ya Basana:
Pakuti cifundo cace ncosatha.
21Ndipo anaperekadzikolaolikhale cosiyira;
Pakuti cifundo cace ncosatha.

22Cosiyira ca kwa Israyeli mtumiki wace;
Pakuti cifundo cace ncosatha.
23Amene anatikumbukila popepuka ife;
Pakuti cifundo cace ncosatha.
24Natikwatula kwa otisautsa;
Pakuti cifundo cace ncosatha.
25Ndiye wakupatsa nyama zonse cakudya;
Pakuti cifundo cace ncosatha.
26Yamikani Mulungu wa kumwamba,
Pakuti cifundo cace ncosatha.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 137

Kudandaula kwa Ayuda ku Babulo

1Ku mitsinje ya ku Babulo,
Kumeneko tinakhala pansi, inde tinalira,
Pokumbukila Ziyoni.
2Pa msondodzi uli m'mwemo Tinapacika mazeze athu.
3Popeza pamenepo akutigwirawo anatifunsa nyimbo,
Ndipo akutizunza anafuna tisekere,
Ndi kuti, Mutiyimbire nyimbo imodzi ya ku Ziyoni.
4Tidati, Tidzayimba bwanji nyimbo ya Yehova
M'dziko lacilendo?
5Ndikakuiwalani, Yerusalemu,
Dzanja lamanja langa liiwale luso lace.
6Lilime langa limamatike ku nsaya zanga,
Ndikapanda kukumbukila inu;
Ndikapanda kusankha Yerusalemu
Koposa cimwemwe canga copambana.
7Yehova, kumbukilani ana a Edomu
Tsiku la Yerusalemu;
Amene adati, Gamulani, gamulani,
Kufikira maziko ace.
8Mwana wamkazi wa ku Babulo, iwe amene udzapasulidwa;
Wodala iye amene adzakubwezera cilango
Monga umo unaticitira ife.
9Wodala iye amene adzagwira makanda ako,
Ndi kuwaphwanya pathanthwe.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 138

Davide ayamika Mulungu pa kukhulupirika kwace, naneneratu kuti mafumu onse adzatero

Salmo la Davide.

1Ndidzakuyamikani ndi mtima wangawonse;
Ndidzayimba zakukulemekezani patsogolo pa milungu,
2Ndidzagwadira kuloza ku Kacisi wanu woyera,
Ndi kuyamika dzina lanu,
Cifukwa ca cifundo canu ndi coonadi canu;
Popeza munakuzitsa mau anu koposa dzina lanu lonse.
3Tsiku loitana ine, munandiyankha,
Munandilimbitsa ndi mphamvu m'moyo mwanga.
4Mafumu onse a pa dziko lapansi adzakuyamikani,
Yehova, popeza adamva mau a pakamwa panu.
5Ndipo adzayimbira njira za Yehova;
Pakuti ulemerero wa Yehova ndi waukuru.
6Angakhale Yehova ngwokwezeka, apenyanso wopepukayo;
Koma wodzikuza amdziwira kutali.
7Ndingakhale ndiyenda pakati pa nsautso, mudzandipatsa moyo;
Mudzatambasula dzanja lanu pa mkwiyo wa adani anu,
Ndipo dzanja lanu lamanja lidzandipulumutsa.
8Yehova adzanditsirizira za kwa ine:
Cifundo canu, Yehova, cifikira ku nthawi zonse:
Musasiye nchito za manja anu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 139

Mulungu ali ponse ponse, adziwa zonse

Kwa Mkulu wa Nsembe. Salmo la Davide.

1Munandisanthula, Yehova, nimundidziwa.
2Inumudziwakukhalakwangandi kuuka kwanga,
Muzindikira lingaliro langa muli kutali.
3Muyesa popita ine ndi pogona ine,
Ndi njira zanga zonse muzolowerana nazo.
4Pakuti asanafike mau pa lilime langa,
Taonani, Yehova, muwadziwa onse.
5Munandizinga kumbuyo ndi kumaso,
Nimunaika dzanja lanu pa ine.
6Kudziwa ici kundilaka ndi kundidabwiza:
Kundikhalira patali, sindifikirako.
7Ndidzapita kuti kuzembera mzimu wanu?
Kapena ndidzathawira kuti kuzembera nkhope yanu?
8Ndikakwera kumka kumwamba, muli komweko;
Kapena ndikadziyalira ku Gehena, taonani, muli komweko.
9Ndikadzitengera mapiko a mbanda kuca,
Ndi kukhala ku malekezero a nyanja;
10Kungakhale komweko dzanja lanu lidzanditsogolera,
Nilidzandigwira dzanja lanu lamanja.
11Ndipo ndikati, Koma mdima undiphimbe,
Ndi kuunika kondizinga kukhale usiku:
12Ungakhale mdima sudetsa pamaso panu,
Koma usiku uwala ngati usana:
Mdima ukunga kuunika.
13Pakuti Inu munalenga imso zanga;
Munandiumba ndisanabadwe ine.
14Ndikuyamikani cifukwa kuti cipangidwe canga ncoopsa ndi codabwiza;
Nchito zanu nzodabwiza;
Moyo wanga ucidziwa ici bwino ndithu.
15Thupi langa silinabisikira Inu popangidwa ine mobisika,
Poombedwa ine monga m'munsi mwace mwa dziko lapansi.
16Ndisanaumbidwe ine maso anu anandipenya,
Ziwalo zanga zonse zinalembedwa m'buku mwanu,
Masiku akuti ziumbidwe, Pakalibe cimodzi ca izo.
17Potero, Mulungu, ndiziyesa zolingalira zanu za mtengo wace ndithu!
Mawerengedwe ace ndi ambirimbiri!
18Ndikaziwerenga zicuruka koposa mcenga:
Ndikauka ndikhalanso nanu.
19Indedi, mudzaomba woipa, Mulungu:

Ndipo amuna inu nkhumba mwazi, cokani kwa ine.
20Popeza anena za Inu moipa,
Ndi adani anu achula dzina lanu mwacabe.
21Kodi sindidana nao iwo akudana ndi Inu, Yehova?
Ndipo kodi sindimva nao cisoni iwo akuukira Inu?
22Ndidana nao ndi udani weni weni:
Ndiwayesa adani.
23Mundisanthule, Mulungu, nimudziwe mtima wanga;
Mundiyese nimudziwe zolingalira zanga.
24Ndipo mupenye ngati ndiri nao mayendedwe oipa,
Nimunditsogolere pa njira yosatha.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 140

Davide apempha Mulungu amlanditse kwa mdani woipa wamphamvu

Kwa Mkulu wa nsembe; Salmo la Davide.

1Ndilanditseni, Yehova, kwa munthu woipa;
Ndisungeni kwa munthu waciwawa;
2Amene adzipanga zoipa mumtima mwao;
Masiku onse amemeza nkhondo. 3Anola lilime lao ngati njoka;
Pansi pa milomo yao pali ululu wa mphiri.
4Ndilindireni Yehova, ndisalowe m'manja mwa woipa;
Ndisungeni kwa munthu waciwawa;
Kwa iwo akuti akankhe mapazi anga.
5Odzikuzaanandichera msampha, nandibisira zingwe;
Anacha ukonde m'mphepete mwa njira;
Anandichera makwekwe.
6Ndinati kwa Yehova, Inu ndinu Mulungu wanga;
Mundicherere khutu mau a kupemba kwanga, Yehova.
7Yehova Ambuye, ndinu mphamvu ya cipulumutso canga,
Munandiphimba mutu wanga tsiku lakulimbana nkhondo.
8Yehova, musampatse woipa zokhumba iye;
Musamthandize zodzipanga zace; angadzikuze.
9Kunena za mutu wao wa iwo akundizinga,
Coipa ca milomo yao ciwaphimbe.
10Makala amoto awagwere;
Aponyedwe kumoto;
M'maenje ozama, kuti asaukenso.
11Munthu wamlomo sadzakhazikika pa dziko lapansi;
Coipa cidzamsaka munthu waciwawa kuti cimgwetse.
12Ndidziwa kuti Yehova adzanenera wozunzika mlandu,
Ndi kuweruzira aumphawi,
13Indedi, olungama adzayamika dzina lanu;
Oongoka mtima adzakhala pamaso panu,

©The Bible Society of Malawi, 1992

Davide apempha Mulungu amthandize poyesedwa ndi zoipa

Salmo la Davide.

1Yehova, ndaitana kwa Inu; ndifulumireni ine;
Mundicherere khutu, pamene ndiitana kwa Inu.
2Pempherolanga liikike ngaticofukiza pamaso panu;
Kukweza manja anga kuikike ngati nsembe ya madzulo.
3Muike mdindo pakamwa panga, Yehova;
Sungani pakhomo pa milomo yanga.
4Mtima wanga usalinge ku cinthu coipa,
Kucita nchito zoipa
Ndi anthu akucita zopanda pace;
Ndipo ndisadye zankhuli zao.
5Akandipanda munthu wolungama ndidzati ncifundo:
Akandidzudzula, ndidzakuyesa mafuta a pamutu;
Mutu wanga usakane:
Pakuti pangakhale posautsidwa iwo ndidzawapempherera.
6Oweruza ao anagwetseka pambali pa thanthwe;
Nadzamva mau anga kuti ndiwo okondweretsa.
7Mafupa athu amwazika pakamwa pa manda,
Monga ngati akumba nanyimphula nthaka yapansi.
8Pakuti maso anga apenya kwanu, Yehova Ambuye;
Ndithawira kwa Inu; musataye moyowanga.
9Mundisunge ndisagwe mumsampha anandicherawo,
Ndisakodwe m'makwekwe a iwo ocita zopanda pace,
10Oipa agwe pamodzi m'maukonde ao,
Kufikira nditapitirira ine.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 142

Pemphero pakuopsedwa kwakukuru

Cilangizo ca Davide, muja anakhala m'phanga; Pemphero,

1Ndipfuula nalo liu langa kwa Yehova;
Ndi mau anga ndipemba kwa Yehova.
2Nditsanulirakudandaulakwanga pamaso pace;
Ndionetsa msauko wanga pamaso pace.
3Pamene mzimu wanga unakomoka m'kati mwanga, munadziwa njira yanga.
M'njira ndiyendamo anandichera msampha,
4Penyani ku dzanja lamanja ndipo muone; palibe wondidziwa;
Pothawirapo pandisowa; palibe mmodzi wosamalira moyo wanga.
5Ndinapfuulira kwa inu, Yehova;
Ndina, Inu ndinu pothawirapo panga,
Gawo langa m'dziko la amoyo.
6Tamverani kupfuula kwanga; papeza ndisauka kwambiri;
Ndilanditseni kwa iwo akundilondola; popeza andilaka.
7Turutsani moyo wanga m'ndende, kuti ndiyamike dzina lanu;
Olungama adzandizinga;
Pakuti mudzandicitira zokoma.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Davide apempha Mulungu amlanditse msanga kwa adani ace

Salmo la Davide.

1Imvani pemphero langa, Yehova; ndicherere khutu kupemba kwanga;
Ndiyankheni mwa cikhulupiriko canu, mwa cilungamo canu.
2Ndipo musaitane mlandu wa mtumiki wanu;
Pakuti pamaso panu sipadzakhala wolungama wamoyo mmodzi yense.
3Pakuti mdani alondola moyo wanga;
Apondereza pansr moyo wanga;
Andikhalitsa mumdima monga iwo adafa kale lomwe.
4Potero mzimu wanga wakomoka mwa ine;
Mtima wanga utenga nkhawa m'kati mwanga,
5Ndikumbukila masiku a kale lomwe;
Zija mudazicita ndilingirirapo;
Ndikamba pa ndekha za nchito ya manja anu.
6Nditambalitsira manja anga kwa Inu:
Moyo wanga ulira Inu monga dziko lolira mvula.
7Fulumirani ndiyankheni, Yehova; mzimu wanga ukutha.
Musandibisire nkhope yanu;
Ndingafanane nao akutsikira kudzenje.
8Mundimvetse cifundo canu mamawa;
Popeza ndikhulupirira Inu:
Mundidziwitse njira ndiyendemo;
Popeza ndikweza moyo wanga kwa Inu.
9Mundilanditse kwa adani anga, Yehova;
Ndibisala mwa Inu.
10Mundiphunzitse cokonda Inu; popeza Inu ndinu Mulungu wanga;
Mzimu wanu ndi wokoma; munditsogolere kucidikha.
11Mundipatse moyo, Yehova, cifukwa ca dzina lanu;
Mwa cilungamo canu muturutse moyo wanga m'nsautso.
12Ndipo mwa cifundo canu mundidulire adani anga,
Ndipo muononge onse akusautsa moyo wanga;
Pakuti ine ndine mtumiki wanu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 144

Davide ayamika Mulungu kuti anamcinjiriza, napempha ampulumutse kuti anthu adalenso

Salmo la Davide.

1Wolemekezeka Yehova thanthwe langa,
Wakuphunzitsa manja anga acite nkhondo,
Zala zanga zigwirane nao:
2Ndiye cifundo canga, ndi linga langa,
Msanje wanga, ndi mpulumutsi wanga;
Cikopa canga, ndi Iye amene ndimtama;
Amene andigonjetsera anthu anga.
3Yehova, munthu ndani kuti mumdziwa?
Mwana wa munthu kuti mumsamalira?
4Munthu akunga mpweya;
Masiku ace akunga mthunzi wopitirira.
5Weramutsani thambo lanu, Yehova, nimutsike:
Khudzani mapiri ndipo adzafuka.
6Ng'animitsani mphezi, ndi kuwabalalitsa;
Tumizani mibvi yanu, ndi kuwapitikitsa,
7Turutsani manja anu kucokera m'mwamba;
Ndikwatuleni ndi kundilanditsa ku madzi akuru,
Ku dzanja la alendo;
8Amene pakamwa pao alankhula zacabe,
Ndi dzanja lao lamanja ndilo dzanja lacinyengo.
9Ndidzakuyimbirani nyimbo yatsopano, Mulungu;
Pa cisakasa ca zingwe khumi ndidzayimbira zakukulemekezani.
10Ndiye amene apatsa mafumu cipulumutso:
Amene alanditsa Davide mtumiki wace ku lupanga loipa.
11Ndilanditseni ndi kundipulumutsa ku dzanja la alendo,
Amene pakamwa pao alankhula zacabe,
Ndi dzanja lao lamanja ndilo dzanja lacinyengo.
12Kuti ana athu amuna akhale ngati mmera udakula usanakhwime;
Ana athu akazi ngati nsanamira za kungondya, zosema zikometsere nyumba ya mfumu.
13Kuti nkhokwe zathu zidzale, kutipatsa za mitundu mitundu;
Ndi kuti nkhosa zathu ziswane zikwi zikwi, inde zikwi khumi kubusako.
14Kuti ng'ombe zathu zikhale zasenza katundu;
Ndi kuti pasakhale kupasula linga kapena kuturukamo,
Pasakhalenso kupfuula m'makwalala athu.
15Odala anthu akuona zotere; Odala anthu amene Mulungu wao ndi Yehova.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Ukuru ndi ukoma wa Mulungu

Salmo lolemekeza; la Davide,

1Ndidzakukwezani Mulungu wanga, Mfumu;
Ndipo ndidzalemekeza dzina lanu ku nthawi za nthawi.
2Masiku onse ndidzakuyamikani;
Ndi kulemekeza dzina lanu ku nthawi za nthawi.
3Yehova ndi wamkulu, nayenera kulemekezedwa kwakukuru;
Ndi ukulu wace ngwosasanthulika.
4Mbadwo wina udzalemekezera nchito zanu mbadwo unzace,
Ndipo udzalalikira zamphamvu zanu.
5Ndidzalingalira ulemerero waukuru wa ulemu wanu,
Ndi nchito zanu zodabwiza.
6Ndipo adzanenera mphamvu za nchito zanu zoopsa;
Ndi ukulu wanu ndidzaufotokozera.
7Adzabukitsa cikumbukilo ca ubwino wanu waukuru,
Nadzayimbira cilungamo canu.
8Yehova ndiye wacisomo, ndi wacifundo;
Osakwiya msanga, ndi wa cifundo cacikuru.
9Yehova acitira cokoma onse;
Ndi nsoni zokoma zace zigwera nchito zace zonse.
10Nchito zanu zonse zidzakuyamikani, Yehova;
Ndi okondedwa anu adzakulemekezani.
11Adzanenera ulemerero wa ufumu wanu,
Adzalankhulira mphamvu yanu;
12Kudziwitsa ana a anthu zamphamvu zace,
Ndi ulemerero waukuru wa ufumu wace.
13Ufumu wanu ndiwo ufumu womka muyaya,
Ndi kuweruza kwanu kufikira mibadwo yonse yonse.
14Yehova agwiriziza onse akugwa,
Naongoletsa onse owerama.
15Maso a onse ayembekeza Inu;
Ndipo muwapatsa cakudya cao m'nyengo zao.
16Muniowetsa dzanja lanu,
Nimukwaniritsira zamoyo zonse cokhumba cao.
17Yehova ali wolungama m'njira zace zonse,
Ndi wacifundo m'nchito zace zonse.
18Yehova ali pafupi ndi onse akuitanira kwa Iye,
Onse akuitanira kwa Iye m'coonadi.
19Adzacita cokhumba iwo akumuopa;
Nadzamva kupfuula kwao, nadzawapulumutsa.
20Yehova asunga onse akukondana naye;
Koma oipa onse adzawaononga.
21Pakamwa panga padzanena cilemekezo ca Yehova;

Ndi zinthu zonse zilemekeze dzina lace loyera ku nthawi za nthawi.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 146

Cifoko ca munthu, cikhulupiriko ca Mulungu

1Haleluya;
Ulemekeze Yehova, moyo wanga,
2Ndidzalemekeza Yehovam'moyo mwanga;
Ndidzayimbira zomlemekeza Mulungu wanga pokhala ndi moyo ine.
3Musamakhulupirira zinduna,
Kapena mwana wa munthu, amene mulibe cipulumutso mwa iye.
4Mpweya wace ucoka, abwerera kumka ku nthaka yace;
Tsiku lomwelo zotsimikiza mtima zace zitayika.
5Wodala munthu amene akhala naye Mulungu wa Yakobo kuti amthandize,
Ciyembekezo cace ciri pa Yehova, Mulungu wace;
6Amene analenga zakumwamba ndi dziko lapansi,
Nyanja ndi zonse ziri m'mwemo;
Ndiye wakusunga coonadi kosatha:
7Ndiye wakucitira ciweruzo osautsika;
Ndiye wakupatsa anjala cakudya;
Yehova amasula akaidi;
8Yehova apenyetsa osaona;
Yehova aongoletsa onse owerama;
Yehova akonda olungama;
9Yehova asunga alendo;
Agwiriziza mwana wamasiye mkazi wamasiye;
Koma akhotetsa njira ya oipa.
10Yehova adzacita ufumu kosatha,
Mulungu wako, Ziyoni, ku mibadwo mibadwo.
Haleluya.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Alemekeze dzina la Mulungu cifukwa ca zokoma amacitira anthu ace

1Haleluya;
Pakuti kuyimbira zomlemekeza Mulungu wathu nkokoma;
Pakuti cikondwetsa ici, cilemekezo ciyenera.
2Yehova amanga Yerusalemu;
Asokolotsa otayika a Israyeli.
3Aciritsa osweka mtima,
Namanga mabala ao.
4Awerenga nyenyezi momwe ziri;
Azicha maina zonsezi.
5Ambuye wathu ndi wamkuru ndi wa mphamvu zambiri;
Nzeru yace njosatha.
6Yehova agwiriziza ofatsa;
Atsitsira oipa pansi.
7Yamikani Yehova ndi kuthira mang'ombe;
Myimbireni Mulungu wathu zamlemekeza pazeze:
8Amene aphimba thambo ndi mitambo,
Amene akonzera mvula nthaka,
Amene aphukitsa msipu pamapiri.
9Amene apatsa zoweta cakudya cao,
Ana a khungubwi alikulira.
10Mphamvu ya kavalo siimkonda:
Sakondwera nayo miyendo ya munthu.
11Yehova akondwera nao akumuopa Iye,
Iwo akuyembekeza cifundo cace.
12Yerusalemu, lemekezani Yehova;
Ziyoni, lemekezani Mulungu wanu.
13Popeza analimbitsa mipiringidzo ya zitseko zanu:
Anadalitsa ana anu m'kati mwanu.
14Ndiyeamene akhalitsamalireanu mumtendere;
Akukhutitsani ndi tirigu wakuca bwino.
15Atumiza lamulo lace ku dziko lapansi;
Mau ace athamanga liwiro.
16Apatsa cipale cofewa ngati ubweya;
Awaza cisanu ngati phulusa.
17Aponya matalala ace ngati zidutsu:
Adzaima ndani pa kuzizira kwace?
18Atumiza mau ace nazisungunula;
Aombetsa mphepo yace, ayenda madzi ace.
19Aonetsa mau ace kwa Yakobo;
Malemba ace, ndi maweruzo ace kwa Israyeli.
20Sanatero nao anthu amtundu wina;
Ndipo za maweruzo ace, sanawadziwa.
Haleluya.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 148

Zolengedwa zonse zilemekeze Mulungu

1Haleluya.
Lemekezani Yehova kocokera kumwamba;
Mlemekezeni m'misanje.
2Mlemekezeni, angelo ace onse;
Mlemekezeni, makamu ace onse.
3Mlemekezeni, dzuwa ndi mwezi;
Mlemekezeni, nyenyezi zonse zaunikira.
4Mlemekezeni, m'mwambamwamba,
Ndi madzi inu, a pamwamba pa thambo.
5Alemekeze dzina la Yehova;
Popeza analamulira, ndipo zinalengedwa.
6Anazikhazikanso ku nthawi za nthawi;
Anazipatsa cilamulo cosatumphika.
7Lemekezani Yehova kocokera ku dziko lapansi,
Zinsomba inu, ndi malo ozama onse;
8Moto ndi matalala, cipale cofewa ndi nkhungu;
Mphepo ya namondwe, yakucita mau ace;
9Mapiri ndi zitunda zonse;
Mitengo yazipatso ndi yamikungudza yonse:
10Nyama za kuthengo ndi zoweta zonse;
Zokwawa, ndi mbalame zakuuluka;
11Mafumu a padziko ndi mitundu yonse ya anthu;
Zinduna ndi oweruza onse a padziko;
12Anyamata ndiponso anamwali;
Okalamba pamodzi ndi ana:
13Alemekeze dzina la Yehova;
Pakuti dzina lace lokha ndi lokwezeka;
Ulemerero wace uli pamwamba pa dziko lapansi ndi thambo.
14Ndipo anakweza nyanga ya anthu ace,
Cilemekezo ca okondedwa ace onse;
Ndiwo ana a Israyeli, anthu a pafupi pa Iye,
Haleluya,

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 149

Okhulupirira onse alemekeze Mulungu wao

1Haleluya,
Myimbireni Yehova nyimbo yatsopano,
Ndi cilemekezo cace mu msonkhano wa okondedwa ace.
2Akondwere Israyeli mwa Iye amene anamlenga;
Ana a Ziyoni asekere mwa Mfumu yao.
3Alemekeze dzina lace ndi kuthira mang'ombe;
Amyimbire zomlemekeza ndi lingaka ndi zeze.
4Popeza Yehova akondwera nao anthu ace;
Adzakometsa ofatsa ndi cipulumutso,
5Okondedwa ace atumphe mokondwera m'ulemu:
Apfuule mokondwera pamakama pao,
6Nyimbo zakukweza Mulungu zikhale pakamwa pao,
Ndi lupanga lakuthwa konse konse m'dzanja lao;
7Kubwezera cilango akunja,
Ndi kulanga mitundu ya anthu;
8Kumanga mafumu ao ndi maunyolo,
Ndi omveka ao ndi majerejede acitsulo;
9Kuwacitira ciweruzo colembedwaco:
Ulemu wa okondedwa ace onse ndi uwu.
Haleluya.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masalmo 150

Zolengedwa zonse zilemekeze Mulungu

1Haleluya,
Lemekezani Mulungu m'malo ace oyera;
Mlemekezeni m'thambo la mphamvu yace.
2Mlemekezeni cifukwa ca nchito zace zolimba;
Mlemekezeni monga mwa ukulu wace waunjinji.
3Mlemekezeni ndi kulira kwa lipenga;
Mlemekezeni ndi cisakasa ndi zeze.
4Mlemekezeni ndi lingaka ndi kuthira mang'ombe:
Mlemekezeni ndi zoyimbira za zingwe ndi citoliro.
5Mlemekezeni ndi nsanje zomveka:
Mlemekezeni ndi nsanje zoliritsa.
6Zonse zakupuma zilemekeze Yehova.
Haleluya.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Proverbs

Miyambi 1

Zocitira miyambi

1MIYAMBI ya Solomo mwana wa Davide, mfumu ya Israyeli.
2Kudziwa nzeru ndi mwambo;
Kuzindikira mau ozindikiritsa;
3Kulandira mwambo wakusamalira macitidwe,
Cilungamo, ciweruzo ndi zolunjika;
4Kucenjeza acibwana,
Kuphunzitsa mnyamata kudziwa ndi kulingalira;
5Kuti wanzeru amve, naonjezere kuphunzira;
Ndi kuti wozindikira afikire kuuphungu;
6Kuzindikira mwambi ndi tanthauzo lace,
Mau a anzeru, ndi zophiphiritsa zao.

Munthu asalole oipa amcete

7Kuopa Yehova ndiko ciyambi ca kudziwa;
Opusa anyoza nzeru ndi mwambo.
8Mwananga, tamva mwambo wa atate wako,
Ndi kusasiya cilangizo ca amako
9Pakuti izi ndi korona wa cisomo pamtu pako,
Ndi mkanda pakhosi pako.
10Mwananga, akakukopa ocimwa usalole.
11Akanena, Idza nafe, tibisalire mwazi,
Tilalire osacimwa opanda cifukwa;
12Tiwameze ali ndi moyo ngati manda,
Ali amphumphu, ngati akutsikira kudzenje;
13Tidzapeza cuma conse ca mtengo wace,
Tidzadzaza nyumba zathu ndi zofunkha;
14Udzacita nafe maere,
Tonse tidzakhala ndi cibeti cimodzi;
15Mwananga, usayende nao m'njira;
Letsa phazi lako ku mayendedwe ao;
16Pakuti mapazi ao athamangira zoipa,
Afulumira kukhetsa mwazi.
17Pakuti kuchera msampha pamaso pa mbalame ndi cabe;
18Ndipo awa abisalira mwazi wao wao, alalira miyoyo yao yao.
19Mayendedwe a yense wopindula cuma monyenga ngotere;
Cilanda moyo wa eni ace,

Ceniezo la Nzeru

20Nzeru ipfuula panja;
Imveketsa mau ace pabwalo;
21Iitana posonkhana anthu polowera pacipata;
M'mudzi inena mau ace;

22Kodi mudzakonda zacibwana kufikira liti, acibwana inu?
Onyoza ndi kukonda kunyoza,
Opusa ndi kuda nzeru?
23Tembenukani pamene ndikudzudzulani;
Taonani, nditsanulira pa inu mzimu wanga,
Ndikudziwitsani mau anga.
24Cifukwa ndaitana, ndipo munakana;
Ndatambasula dzanja langa, ndipo panalibe analabadira;
25Koma munapeputsa uphungu wangawonse,
Ndi kukana kudzudzula kwanga.
26Inetu ndidzacitiraciphwete tsoka lanu,
Ndidzatonyola pakudza mantha anu;
27Pakudza mantha anu ngati mphepo yopasula,
Ndi pofika tsoka lanu ngati kabvumvulu;
Pakudza kwa inu bvuto ndi nsautso.
28Pamenepo adzandiitana, koma sindidzabvomera;
Adzandifunatu, osandipeza ai;
29Cifukwa anada nzeru,
Sanafuna kuopa Yehova;
30Anakana uphungu wanga,
Nanyoza kudzudzula kwanga konse;
31Momwemo adzadya zipatso za mayendedwe ao,
Nadzakhuta zolingalira zao.
32Pakuti kubwerera m'mbuyo kwa acibwana kudzawapha;
Ndipo mphwai za opusa zidzawaononga.
33Koma wondimvera ine adzakhala osatekeseka,
Nadzakhala phe osaopa zoipa,

©The Bible Society of Malawi, 1992

Ukoma ndi phindu tace la Nzeru

1Mwananga, ukalandira mau anga,
Ndi kusunga malamulo anga;
2Kucherera makutu ako kunzeru,
Kulozetsa mtima wako kukuzindikira;
3Ukaitananso luntha,
Ndi kupfuulira kuti ukazindikire;
4Ukaifunafuna ngati siliva,
Ndi kuipwaira ngati cuma cobisika;
5Pompo udzazindikira kuopa Yehova
Ndi kumdziwadi Mulungu.
6Pakuti Yehova apatsa nzeru;
Kudziwa ndi kuzindikira kuturuka m'kamwa mwace;
7Iye asungira oongoka mtima nzeru yeniyeni;
Ndiye cikopa ca oyenda molunjika;
8Kuti acinjirize njira za ciweruzo,
Nadikire khwalala la opatulidwa ace.
9Pamenepo udzazindikira cilungamo ndi ciweruzo,
Zolunjika ndi mayendedwe onse abwino.
10Pakuti nzeru idzalowa m'mtima mwako,
Moyo wako udzakondwera ndi kudziwa,
11Kulingalira kudzakudikira,
Kuzindikira kudzakucinjiriza;
12Kukupulumutsa ku njira yoipa,
Kwa anthu onena zokhota;
13Akusiya mayendedwe olungama,
Akayende m'njira za mdima;
14Omwe asangalala pocita zoipa,
Nakondwera ndi zokhota zoipa;
15Amene apotoza njira zao,
Nakhotetsa mayendedwe ao;
16Nzeru idzakupulumutsa kwa mkazi waciwerewere,
Kwa mkazi wacilendo wosyasyalika ndi mau ace;
17Wosiya bwenzi la ubwana wace,
Naiwala cipangano ca Mulungu wace;
18Nyumba yace itsikira kuimfa,
Ndi mayendedwe ace kwa akufa;
19Onse akunka kwa iye sabweranso,
Safika ku njira za moyo;
20Nzeru idzakuyendetsa m'njira ya anthu abwino,
Kuti usunge mayendedwe a olungama.
21Pakuti oongoka mtima adzakhala m'dziko,
Angwiro nadzatsalamo.

22Koma oipa adzalikhidwa m'dziko,
Aciwembu adzazulidwamo.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Malangizo a kuopa, kukhulupira, ndi kumvera Yehova

1Mwananga, usaiwale malamulo anga,
Mtima wako usunge malangizo anga;
2Pakuti adzakuonjezera masiku ambiri,
Ndi zaka za moyo ndi mtendere.
3Cifundo ndi coonadi zisakusiye;
Uzimange pakhosi pako;
Uzilembe pamtima pako;
4Motero udzapezakisomo ndi nzeru yabwino,
Pamaso pa Mulungu ndi anthu.
5Khulupirira Yehova ndi mtima wako wonse,
Osacirikizika pa luntha lako;
6Umlemekeze m'njira zako zonse,
Ndipo Iye adzaongola mayendedwe ako.
7Usadziyese wekha wanzeru;
Opa Yehova, nupatuke pazoipa;
8Mitsempha yako idzalandirapo moyo,
Ndi mafupa ako uwisi.
9Lemekeza Yehova ndi cuma cako,
Ndi zinthu zako zonse zoyambirira kuca;
10Motero nkhokwe zako zidzangoti the,
Mbiya zako zidzasefuka vinyo.
11Mwananga, usapeputse mwambo wa Yehova,
Ngakhale kutopa ndi kudzudzula kwace;
12Pakuti Yehova adzudzula omwe awakonda;
Monga atate mwana amene akondwera naye.

Phindu la Nzeru

13Wodala ndi wopeza nzeru,
Ndi woona luntha;
14Pakuti malonda a nzeru aposa malonda a siliva,
Phindu lace liposa golidi woyengeka.
15Mtengo wace uposa ngale;
Ndipo zonse zikukondweretsa sizilingana naye.
16Masiku ambiri ali m'dzanja lamanja lace;
Cuma ndi ulemu m'dzanja lace lamanzere.
17Njira zace ziri zokondweretsa,
Mayendedwe ace onse ndiwo mtendere.
18Ndiyo mtengo wa moyo wa akuigwira;
Wakulumirira ngwodala.
19Yehova anakhazika dziko ndi nzeru;
Naika zamwamba ndi luntha.
20Zakuya zinang'ambika ndi kudziwakwace;
Thambo ligwetsa mame.

21Mwananga, zisacokere ku maso ako;
Sunga nzeru yeniyeni ndi kulingalira;
22Ndipo mtima wako udzatengapo moyo,
Ndi khosi lako cisomo.
23Pompo udzayenda m'njira yako osaopa,
Osapunthwa phazi lako.
24Ukagona, sudzacita mantha;
Udzagona tulo tokondweretsa.
25Usaope zoopsya zodzidzimutsa,
Ngakhale zikadza zopasula oipa;
26Pakuti Yehova adzalimbitsa mtima wako,
Nadzasunga phazi lako lingakodwe.

Malangizo ena osiyana

27Oyenera kulandira zabwino usawamane;
Pokhoza dzanja lako kuwacitira zabwino.
28Usanene kwa mnzako, Ukabwerenso,
Ndipo mawa ndidzakupatsa;
Pokhala uli nako kanthu.
29Usapangire mnzako ciwembu;
Popeza akhala nawe pafupi osatekeseka.
30Usakangane ndi munthu cabe,
Ngati sanakucitira coipa,
31Usacitire nsanje munthu waciwawa;
Usasankhe njira yace iri yonse.
32Pakuti wamphulupulu anyansa Yehova;
Koma cinsinsi cace ciri ndi oongoka.
33Mulungu atemberera za m'nyumba ya woipa;
Koma adalitsa mokhalamo olungama.
34Anyozadi akunyoza,
Koma apatsa akufatsa cisomo.
35Anzeru adzalandira ulemu colowa cao;
Koma opusa adzakweza manyazi.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Ceniezo lakuti afune Nzeru nalewe njira za oipa

1Ananu, mverani mwambo wa atate,
Nimuchere makutu mukadziwe luntha;
2Pakuti ndikuphunzitsani zabwino;
Musasiye cilangizo canga.
3Pakuti ndinali mwana kwa atate wanga,
Wokondedwa ndi mai, ndine ndekha, sanabala wina.
4Atate nandiphunzitsa, nati kwa ine,
Mtima wako uumirire mau anga;
Sunga malamulo anga, nukhale ndi moyo.
5Tenga nzeru, tenga luntha;
Usaiwale, usapatuke pa mau a m'kamwa mwanga;
6Usasiye nzeru, ndipo Idzakusunga;
Uikonde, idzakucinjiriza.
7Nzeru ipambana, tatenga nzeru;
M'kutenga kwako konseko utenge luntha.
8Uilemekeze, ndipo idzakukweza;
Idzakutengera ulemu pamene uifungatira.
9Idzaika cisada ca cisomo pamtu pako;
Idzakupatsa korona wokongola.
10Tamvera mwananga, nulandire mau anga;
Ndipo zaka za moyo wako zidzacuruka.
11Ndakuphunzitsa m'njira ya nzeru,
Ndakuyendetsa m'mayendedwe olungama.
12Mapazi ako sadzaombana ulikuyenda;
Ukathamanga, sudzapunthwa.
13Gwira mwambo, osauleka;
Uusunge; pakuti ndiwo moyo wako.
14Usalowe m'mayendedwe ocimwa,
Usayende m'njira ya oipa.
15Pewapo, osapitamo;
Patukapo, nupitirire.
16Pakuti akapanda kucita zoipa, samagona;
Ndipo akapanda kukhumudwitsa wina, tulo tao tiwacokera.
17Pakuti amadya cakudya ca ucimo,
Namwa vinyo wa cifwamba.
18Koma mayendedwe a olungama akunga kuunika kwa mbanda kuca,
Kunkabe kuwala kufikira usana woti mbe.
19Njira ya oipa ikunga mdima;
Sadziwa cimene ciwapunthwitsa,
20Mwananga, tamvera mau anga;
Cherera makutu ku zonena zanga.

21Asacoke ku maso ako;
Uwasunge m'kati mwa mtima wako.
22Pakuti ali moyo kwa omwe awapeza,
Nalamitsa thupi lao lonse.
23Cinjiriza mtima wako koposa zonse uzisunga;
Pakuti magwero a moyo aturukamo.
24Tasiya m'kamwa mokhota,
Uike patari milomo yopotoka.
25Maso ako ayang'ane m'tsogolo,
Zikope zako zipenye moongoka,
26Sinkasinkha bwino mayendedwe a mapazi ako;
Njira zako zonse zikonzeke.
27Usapatuke ku dzanja lamanja kapena kulamanzere;
Suntha phazi lako kusiya zoipa.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Miyambi 5

Acenjere naye mkazi woipa

1Mwananga, mvera nzeru yanga;
Cherera makutu ku luntha langa;
2Ukasunge zolingalira,
Milomo yako ilabadire zomwe udziwa.
3Pakuti milomo ya mkazi waciwerewere ikukha uci;
M'kamwa mwace muti see koposa mafuta.
4Cimariziro cace ncowawa ngati civumulo,
Ndi cakuthwa ngati lupanga lakuthwa konse konse.
5Mayendedwe ace atsikira kuimfa;
Mapazi ace aumirira kumanda;
6Sasinkhasinkha bwino za njira ya moyo;
Mayendedwe ace adzandira dzandi dzandi osadziwa iye.
7Ndipo tsopano ana, mundimvere,
Musapatuke ku mau a m'kamwa mwanga.
8Siyanitsa njira yako kutari kwa iyeyo,
Osayandikira ku khomo la nyumba yace;
9Kuti ungapereke ulemu wako kwa ena,
Ndi zaka zako kwa ankhanza;
10Kuti mphamvu yako isakhutitse alendo,
Ndi kuti usagwire nchito m'nyumba ya wacilendo;
11Ungalire pa cimariziro cako,
Pothera nyama yako ndi thupi lako;
12Ndi kuti, Bwanji ndinada mwambo,
Mtima wanga ndi kunyoza cidzudzulo;
13Ndipo sindinamvera mau a aphunzitsi anga;
Ngakhale kucherera makutu kwa akundilanga mwambo!
14Ndikadakhala m'zoipa zonse,
M'kati mwa msonkhano ndi khamu la anthu.
15Imwa madzi a m'citsime mwako,
Ndi madzi oyenda a m'kasupe mwako.
16Kodi magwero ako ayenera kumwazika kunja,
Ndi mitsinje ya madzi m'makwalala?
17Ikhale ya iwe wekha,
Si ya alendo okhala nawe ai.
18Adalitsike kasupe wako;
Ukondwere ndi mkazi wokula nayo.
19Ngati mbawala yokonda ndi cinkhoma cacisomo,
Maere ace akukwanire nthawi zonse;
Ukodwe ndi cikondi cace osaleka.
20Pakuti ukondwerenji, mwananga, ndi mkazi waciwerewere,
Ndi kufungatira cifuwa ca mkazi wacilendo?
21Pakuti njira za munthu ziri pamaso pa Yehova,

Asinkhasinkha za mayendedwe ace onse.
22Zoipazacezacezidzagwira woipa;
Adzamangidwa ndi zingwe za ucimo wace.
23Adzafa posowa mwambo;
Adzasocera popusa kwambiri.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Za kuperekera mnzace cikole. Zisanu ndi ziwiri zoipira Mulungu

1Mwananga, ngati waperekera mnzako cikole,
Ngati wapangana kulipirira mlendo,
2Wakodwa ndi mau a m'kamwa mwako,
Wagwidwa ndi mau a m'kamwa mwako.
3Cita ici tsono; mwananga, nudzipulumutse;
Popeza walowa m'dzanja la mnzako,
Pita nudzicepetse, numdandaulire mnzako,
4Usaone tulo m'maso mwako,
Ngakhale kuodzera zikope zako.
5Dzipulumutse wekha ngati mphoyo ku dzanja la msaki,
Ndi mbalame ku dzanja la msodzi.
6Pita kunyerere, wolesi iwe,
Penya njira zao nucenjere;
7Ziribe mfumu,
Ngakhale kapitao, ngakhale mkuru;
8Koma zitengeratu zakudya zao m'malimwe;
Nizituta dzinthu zao m'masika.
9Udzagona mpaka liti, wolesi iwe?
Udzauka ku tulo tako liti?
10Tulo ta pang'ono, kuodzera pang'ono,
Kungomanga manja pang'ono, ndi kugona;
11Ndipo umphawi wako udzafika ngati mbala,
Ndi kusauka kwako ngati munthu wacikopa.
12Munthu wopanda pace, mwamuna wamphulupulu;
Amayenda ndi m'kamwa mokhota;
13Amatsinzinira ndi maso ace, napalasira ndi mapazi ace,
Amalankhula ndi zala zace;
14Zopotoka ziri m'mtima mwace, amaganizira zoipa osaleka;
Amapikisanitsa anthu.
15Cifukwa cace tsoka lace lidzadza modzidzimuka;
Adzasweka msanga msanga, palibe compulumutsa.
16Ziripo zinthu zisanu ndi cimodzi Mulungu azida;
Ngakhale zisanu ndi ziwiri zimnyansa:
17Maso akunyada, lilime lonama,
Ndi manja akupha anthu osacimwa;
18Mtima woganizira ziwembu zoipa,
Mapazi akuthamangira mphulupulu mmangu mmangu;
19Mboni yonama yonong'ona mabodza,
Ndi wopikisanitsa abale.
20Mwananga, sunga malangizo a atate wako,
Usasiye malamulo a mako;

21Uwamange pamtima pako osaleka;
Uwalunze pakhosi pako.
22Adzakutsogolera ulikuyenda,
Ndi kukudikira uli m'tulo,
Ndi kulankhula nawe utauka.
23Pakuti malangizo ndi nyali, malamulo ndi kuunika;
Ndi zidzudzulo za mwambo ndizo njira ya moyo;
24Zikucinjiriza kwa mkazi woipa,
Ndi ku lilime losyasyalika la mkazi waciwerewere.
25Asakucititse kaso m'mtima mwako,
Asakukole ndi zikope zace.
26Pakuti ukayamba ndi mkazi wadama, udzamariza ndi nyenyeswa;
Ndipo mkazi wa mwini amasaka moyo wa mtengo wapatari.
27Kodi mwamuna angatenge moto pa cifuwa cace,
Osatentha zobvala zace?
28Pena kodi mwamuna angayende pa makala oyaka,
Osapsya mapazi ace?
29Comweco wolowa kwa mkazi wa mnzace;
Womkhudzayo sadzapulumuka cilango.
30Anthu sanyoza mbala ikaba,
Kuti ikhutitse mtima wace pomva njala;
31Koma ikapezedwa idzabwezera kasanu ndi kawiri;
Idzapereka cuma conse ca m'nyumba yace.
32Wocita cigololo ndi mkazi alibe nzeru;
Wofuna kuononga moyo wace wace ndiye amatero.
33Adzalasidwa nanyozedwa;
Citonzo cace sicidzafafanizidwa.
34Pakuti nsanje ndiyo ukali wa mwamuna,
Ndipo sadzacitira cifundo tsiku lobwezera cilango.
35Sadzalabadira ciombolo ciri conse,
Sadzapembedzeka ngakhale ucurukitsa malipo,

©The Bible Society of Malawi, 1992

Miyambi 7

Acenjere naye mkazi woipa

1Mwananga, sunga mau anga,
Ukundike malangizo anga;
2Sunga malangizo anga, nukhale ndi moyo;
Ndi malamulo anga ngati mwana wa diso lako.
3Uwamange pa zala zako,
Uwalembe pamtima pako;
4Nena kwa nzeru, Ndiwe mlongwanga;
Nuche luntha mbale wako.
5Kuti zikucinjirizire kwa mkazi waciwerewere,
Kwa mlendo wamkazi wosyasyalika ndi mau ace.
6Pakuti pa zenera la nyumba yanga
Ndinapenyera pa made ace;
Ndinaona pakati pa acibwana,
7Ndinazindikira pakati pa ang'ono
Mnyamata wopanda nzeru,
8Alikupita pakhwalala pafupi ndi mphambano ya pa mkaziyo,
Ndi kuyenda pa njira ya ku nyumba yace;
9Pa madzulo kuli sisiro,
Pakati pa usiku pali mdima,
10Ndipo taona, mkaziyo anamcingamira,
Atabvala zadama wocenjera mtima,
11Ali wolongolola ndi wosaweruzika,
Mapazi ace samakhala m'nyumba mwace.
12Mwina ali kumakwalala, mwina ali kumabwalo,
Nabisalira pa mphambano zonse.
13Ndipo anagwira mnyamatayo, nampsompsona;
Nati kwa iye ndi nkhope yacipongwe,
14Nsembe za mtendere ziri nane;
Lero ndacita zowinda zanga.
15Cifukwa cace ndaturuka kudzakucingamira,
Kudzafunitsa nkhope yako, ndipo ndakupeza.
16Ndayala zopfunda pakama panga,
Nsaru zamangamanga za thonje la ku Aigupto,
17Ndakapiza pamphasa panga mankhwala onunkhira
A mvunja ndi cisiyo ndi mtanthanyerere.
18Tiye tikondwere ndi cikondano mpaka mamawa;
Tidzisangalatse ndi ciyanjano.
19Pakuti mwamuna kulibe kwathu,
Wapita ulendo wa kutari;
20Watenga thumba la ndalama m'dzanja lace,
Tsiku lowala mwezi adzabwera kwathu.
21Amkakamiza ndi kukoka kwa mau ace,

Ampatutsa ndi kusyasyalika kwa milomo yace.
22Mnyamatayo amtsata posacedwa, monga ng'ombe ipita
kukaphedwa;
Ndi monga unyolo umadza kulanga citsiru;
23Mpaka mubvi ukapyoza mphafa yace;
Amtsata monga mbalame yotamangira msampha;
Osadziwa kuti adzaononga moyo wace.
24Ndipo tsopano, ananga, mundimvere ine,
Labadirani mau a m'kamwa mwanga.
25Mtima wako usapatukire ku njira ya mkaziyo,
Usasocere m'mayendedwe ace.
26Pakuti amagwetsa ambiri, atawalasa;
Ndipo ophedwa ndi iye acurukadi.
27Nyumba yace ndiyo njira ya kumanda,
Yotsikira ku zipinda za imfa.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Miyambi 8

Nzeru ipambana m'kucita kwace

1Kodi nzeru siitana,
Luntha ndi kukweza mau ace?
2Iima pamwamba pa mtunda,
Pa mphambano za makwalala;
3Pambali pa cipata polowera m'mudzi,
Polowa anthu pa makomo ipfuula:
4Ndinu ndikuitanani, amuna,
Mau anga ndilankhula kwa ana a anthu.
5Acibwana inu, cenjerani,
Opusa inu, khalani ndi mtima wozindikira;
6Imvani, pakuti ndikanena zoposa,
Ndi zolungama potsegula pakamwa panga,
7Pakuti m'kamwa mwanga mudzalankhula ntheradi,
Zoipa zinyansa milomo yanga.
8Mau onse a m'kamwa mwanga alungama;
Mwa iwo mulibe zokhota ndi zopotoka.
9Onsewo amveka ndi iye amene azindikira;
Alungama kwa akupeza nzeru.
10Landirani mwambo wanga, si siliva ai;
Ndi nzeru kopambana ndi golidi wosankhika.
11Pakuti nzeru iposa ngale,
Ndi zonse tizifunitsa sizilingana nayo,
12Ine Nzeru ndikhala m'kucenjera, ngati m'nyumba yanga;
Ndimapeza kudziwa ndi zolingalira.
13Kuopa Yehova ndiko kuda zoipa;
Kunyada, ndi kudzikuza, ndi njira yoipa, ndi m'kamwa mokhota, ndizida.
14Ndine mwini uphungu ndi kudziwitsa;
Ndine luntha; ndiri ndi mphamvu.
15Mwa ine mafumu alamulira;
Akazembe naweruza molungama.
16Mwa ine akalonga ayang'anira,
Ndi akuru, ngakhale oweruza onse a m'dziko,
17Akundikonda ndiwakonda;
Akundifunafuna adzandipeza.
18Katundu ndi ulemu ziri ndi ine,
Cuma cosatha ndi cilungamo.
19Cipatso canga ciposa golidi, ngakhale golidi woyengeka;
Phindu langa liposa siliva wosankhika.
20Ndimayenda m'njira ya cilungamo,
Pakati pa mayendedwe a ciweruzo,
21Kuti ndionetse cuma akundikonda, cikhale colowa cao,

Ndi kudzaza mosungira mwao.
Nzeru ndiyo ya nthawi yosayamba
22Mulungu anali nane poyamba njira yace,
Asanalenge zace zakale.
23Anandiimika cikhalire ciyambire,
Dziko lisanalengedwe.
24Pamene panalibe zozama ndinabadwa ine,
Pamene panalibe akasupe odzala madzi.
25Mapiri asanakhazikike,
Zitunda zisanapangidwe, ndinabadwa;
26Asanalenge dziko, ndi thengo,
Ngakhale ciyambi ca pfumbi la dziko.
27Pamene anakhazika mlengalenga ndinali pompo;
Pamene analemba pazozama kwete kwete;
28Polimbitsa Iye thambo la kumwamba,
Pokula akasupe a zozama.
29Poikira nyanja malire ace,
Kuti madzi asapitirire pa lamulo lace;
Polemba maziko a dziko,
30Ndinali pa mbali pace ngati mmisiri;
Ndinamsekeretsa tsiku ndi tsiku,
Ndi kukondwera pamaso pace nthawi zonse;
31Ndi kukondwera ndi dziko lace lokhalamo anthu,
Ndi kusekerera ndi ana a anthu.
32Ndipo tsopano, ananga, mundimvere ine,
Ngodala akusunga njira zanga.
33Imvani mwambo, mukhale anzeru osaukana.
34Ngwodala amene andimvera, nadikira pa zitseko zanga tsiku ndi tsiku,
Ndi kulinda pa mphuthu za makoma anga;
35Pakuti wondipeza ine apeza moyo;
Yehova adzamkomera mnma.
36Koma wondicimwira apweteka moyo wace;
Onse akundida ine akonda imfa.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Miyambi 9

Madyerero a Nzeru

1Nzeru yamanga nyumba yace,
Yasema zoimiritsa zace zisanu ndi ziwiri;
2Yaphera nyama yace, nisanganiza vinyo wace,
Nilongosolanso pa gome lace.
3Yatuma anamwali ace, iitana
Pa misanje ya m'mudzi.
4Wacibwana yense apambukire kuno;
Iti kwa yense wosowa nzeru,
5Tiyeni, idyani cakudya canga;
Nimumwe vinyo wanga ndamsanganiza.
6Lekani, acibwana inu, nimukhale ndi moyo;
Nimuyende m'njira ya nzeru.
7Woweruza munthu wonyoza adzicititsa yekha manyazi;
Yemwe adzudzula wocimwa angodetsa mbiri yace yace.
8Usadzudzule wonyoza kuti angakude;
Dzudzula wanzeru adzakukonda.
9Ukacenjeza wanzeru adzakulitsa nzeru yace;
Ukaphunzitsa wolungama adzaonjezera kuphunzira,
10Ciyambi ca nzeru ndico kuopa Yehova;
Kudziwa Woyerayo ndiko luntha;
11Pakuti mwa ine masiku ako adzacuruka,
Zaka za moyo wako zidzaonjezedwa.
12Ukakhala wanzeru, si yako yako nzeruyo?
Ndipo ukanyoza udzasauka wekha.
13Utsiru umalongolola,
Ngwa cibwana osadziwa kanthu.
14Ukhala pa khomo la nyumba yace,
Pampando pa misanje ya m'mudzi
15Kuti uitane akupita panjira,
Amene angonkabe m'kuyenda kwao,
16Wacibwana ndani? Apambukire kuno.
Ati kwa yense wopanda nzeru,
17Madzi akuba atsekemera,
Ndi cakudya cobisika cikoma.
18Ndipo mwamunayo sadziwa kuti akufa ali konko;
Omwe acezetsa utsiru ali m'manda akuya.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Miyambo yosiyana-siyana; Miyambo ya Sotomo

1Mwana wanzeru akondweretsa atate;
Koma mwana wopusa amvetsa amace cisoni.
2Cuma ca ucimo sicithangata:
Koma cilungamo cipulumutsa kuimfa.
3Yehova samvetsa njala moyo wa wolungama;
Koma amainga cifuniro ca wocimwa.
4Wocita ndi dzanja laulesi amasauka;
Koma dzanja la akhama lilemeretsa.
5Wokolola m'malimwe ndi mwana wanzeru;
Koma wogona pakututa ndi mwana wocititsa manyazi.
6Madalitso ali pamtu pa wolungama
Koma m'kamwa mwa oipa mubisa ciwawa.
7Amayesa wolungama wodala pamkumbukira;
Koma dzina la oipa lidzabvunda.
8Mwini mtima wanzeru amalandira malamulo;
Koma citsiru colongolola cidzagwa.
9Woyenda moongoka amayenda osatekeseka;
Koma wokhotetsa njira zace adzadziwika.
10Wotsinzinira acititsa cisoni;
Koma wodzudzula momveka acita mtendere.
11M'kamwa mwa wolungama ndi kasupe wa moyo;
Koma m'kamwa mwa oipa mubisa ciwawa.
12Udani upikisanitsa;
Koma cikondi cikwirira zolakwa zonse.
13Nzeru ipezedwa m'milomo ya wozindikira;
Koma wopusa pamsana pace ntyole.
14Anzeru akundika zomwe adziwa
Koma m'kamwa mwa citsiru muononga tsopano lino.
15Cuma ca wolemera ndi mudzi wace wolimba;
Koma umphawi wao uononga osauka.
16Nchito za wolungama zipatsa moyo;
Koma phindu la oipa licimwitsa.
17Wosunga mwambo ali m'njira ya moyo;
Koma wosiya cidzudzulo asocera.
18Wobisa udani ali ndi milomo yonama;
Wonena ugogodi ndiye citsiru.
19Pocuruka mau zolakwa sizisoweka;
Koma wokhala cete acita mwanzeru.
20Lilime la wolungama likunga siliva wosankhika;
Koma mtima wa oipa uli wacabe.
21Milomo ya wolungama imadyetsa ambiri;
Koma zitsiru zimafa posowa nzeru.

22Madalitso a Yehova alemeretsa,
Saonjezerapo cisoni.
23Masewero a citsiru ndiwo kucita zoipa;
Koma masewero a wozindikira ndiwo nzeru.
24Comwe woipa aciopa cidzamfikira;
Koma comwe olungama acifuna cidzapatsidwa.
25Monga kabvumvulu angopita, momwemo woipa kuti zi;
Koma olungama ndiwo maziko osatha.
26Ngati vinyo wowawa m'mano, ndi utsi m'maso,
Momwemo wolesi kwa iwo amene amtuma.
27Kuopa Yehova kutanimphitsa masiku;
Koma zaka za oipa zidzafinimpha,
28Ciyembekezo ca olungama ndico cimwemwe;
Koma cidikiro ca oipa cidzaonongeka.
29Njira ya Yehova ndi linga kwa woongoka mtima;
Koma akucita zoipa adzaonongeka.
30Wolungama sadzacotsedwa konse:
Koma oipa sadzakhalabe m'dziko.
31M'kamwa mwa wolungama mulankhula nzeru;
Koma lilime lokhota lidzadulidwa.
32Milomo ya wolungama idziwa zokondweretsa;
Koma m'kamwa mwa oipa munena zokhota,

©The Bible Society of Malawi, 1992

1Muyeso wonyenga unyansa Yehova;
Koma mulingo wamphumphu umsekeretsa.
2Pakudza kudzikuza padzanso manyazi;
Koma nzeru iri ndi odzicepetsa,
3Kuongoka mtima kwa olungama kuwatsogolera;
Koma kukhota kwa aciwembu kudzawaononga.
4Cuma sicithandiza tsiku la mkwiyo;
Koma cilungamo cipulumutsa kuimfa.
5Cilungamo ca wangwiro cimaongola njira yace;
Koma woipa adzagwa ndi zoipa zace.
6Cilungamo ca oongoka mtima cidzawapulumutsa;
Koma aciwembu adzagwidwa ndi mphulupulu yao.
7Pomwalira woipa cidikiro cace cionongeka;
Ciyembekezo ca ucimo cionongeka.
8Wolungama apulumuka kubvuto;
Woipa nalowa m'malo mwace.
9Wonyoza Mulungu aononga mnzace ndi m'kamwa mwace;
Koma olungama adzapulumuka pakudziwa,
10Olungama akapeza bwino, mudzi usekera;
Nupfuula pakuonongeka oipa.
11Madalitso a olungama akuza mudzi;
Koma m'kamwa mwa oipa muupasula.
12Wopeputsa mnzace asowa nzeru;
Koma wozindikira amatonthola.
13Kazitape woyendayenda amawanditsa zinsinsi;
Koma wokhulupirika mtima abisa mau.
14Popanda upo wanzeru anthu amagwa;
Koma pocuruka aphungu pali cipulumutso.
15Woperekera mlendo cikole adzaphwetekwapo;
Koma wakuda cikole akhala ndi mtendere.
16Mkazi wodekha agwiritsa ulemu;
Aukali nagwiritsa cuma.
17Wacifundo acitira moyo wace zokoma;
Koma wankhanza abvuta nyama yace.
18Woipa alandira malipiro onyenga;
Koma wofesa cilungamo aonadi mphotho,
19Wolimbikira cilungamo alandira moyo;
Koma wolondola zoipa adzipha yekha,
20Okhota mtima anyansa Yehova;
Koma angwiro m'njira zao amsekeretsa.
21Zoonadi, wocimwa sadzapulumuka cilango;
Koma mbeu ya olungama idzalanditsidwa.
22Monga cipini cagolidi m'mphuno ya nkhumba,

Momwemo mkazi wokongola wosasinkhasinkha bwino.
23Cifuniro ca olungama cifikitsa zabwino zokha;
Koma ciyembekezo ca oipa mkwiyo.
24Alipo wogawira, nangolemerabe;
Aliponso womana comwe ayenera kupatsa nangosauka.
25Mtima wa mataya udzalemera;
Wothirira madzi nayenso adzathiriridwa.
26Womana tirigu anthu amtemberera;
Koma madalitso adzakhala pamtu pa wogulitsa.
27Wopwaira ubwino afunitsa cikondwerero;
Koma zoipa zidzamfikira wozilondola.
28Wokhulupmra cuma cace adzagwa;
Koma olungama adzaphuka ngati tsamba.
29Wobvuta banja lace adzalowa m'zomsautsa;
Wopusa adzatumikira wanzeru.
30Cipatso ca wolungama ndi mtengo wa moyo;
Ndipo wokola mtima ali wanzeru.
31Taonani, wolungama adzalandira mphotho kunja kuno;
Koposa kotani woipa ndi wocimwa?

©The Bible Society of Malawi, 1992

1Wokonda mwambo akonda kudziwa;
Koma wakuda cidzudzulo apulukira.
2Yehova akomera mtima munthu wabwino;
Koma munthu wa ziwembu amtsutsa,
3Munthu sadzakhazikika ndi udio,
Muzu wa olungama sudzasunthidwa.
4Mkazi wodekha ndiye korona wa mwamuna wace;
Koma wocititsa manyazi akunga cobvunditsa mafupa a mwamunayo.
5Maganizo a olungama ndi ciweruzo;
Koma uphungu wa oipa unyenga.
6Mau a oipa abisalira mwazi;
Koma m'kamwa mwa olungama muwalanditsa.
7Oipa amagwa kuli zi;
Koma banja la olungama limaimabe.
8Munthu amatamandidwa monga mwa nzeru yace;
Koma wokhota mtima adzanyozedwa.
9Wonyozedwa, amene ali ndi kapolo,
Aposa wodzikuza, amene asowa zakudya.
10Wolungama asamalira moyo wa coweta cace;
Koma cifundo ca oipa ndi nkhanza.
11Zakudyazikwanira wolima minda yace;
Koma wotsata anthu opanda pace asowa nzeru.
12Woipa akhumba cokodwa ndi amphulupulu;
Koma muzu wa olungama umabala zipatso.
13M'kulakwa kwa milomo muli msampha woipa;
Koma wolungama amaturuka m'mabvuto.
14Munthu amakhuta zabwino ndi zipatso za m'kamwa mwace;
Zocita za manja ace zidzabwezedwa kwa iye.
15Njira ya citsiru nlolungama pamaso pace pace;
Koma wanzeru amamvera uphungu.
16Mkwiyo wa citsiru udziwika posacedwa;
Koma wanzeru amabisa manyazi.
17Wolankhula ntheradi aonetsa cilungamo;
Koma mboni yonama imanyenga.
18Alipo wonena mwansontho ngati kupyoza kwa lupanga;
Koma lilime la anzeru lilamitsa.
19Mlomo wa ntheradi ukhazikika nthawi zonse;
Koma lilime lonama likhala kamphindi.
20Cinyengo ciri m'mitima ya oganizira zoipa;
Koma aphungu a mtendere amakondwa.
21Palibe bvuto lidzagwera wolungama;
Koma amphulupulu adzadzazidwa ndi zoipa,

22Milomo yonama inyansa Yehova;
Koma ocita ntheradi amsekeretsa.
23Munthu wanzeru abisa zomwe adziwa;
Koma mtima wa opusa ulalikira utsiru.
24Dzanja la akhama lidzalamulira;
Koma wolesi adzakhala ngati kapolo,
25Nkhawa iweramitsa mtima wa munthu;
Koma mau abwino aukondweretsa.
26Wolungama atsogolera mnzace;
Koma njira ya oipa iwasokeretsa.
27Wolesi samaocha nyama yace anaigwira;
Koma wolungama amalandira cuma copambana ca anthu.
28M'khwalala la cilungamo muli moyo;
M'njira ya mayendedwe ace mulibe imfa.

©The Bible Society of Malawi, 1992

1Mwana wanzeru amamvera mwambo wa atate;
Koma wonyoza samvera cidzudzulo.
2Munthu adzadya zabwino ndi zipatso za m'kamwa mwace;
Koma moyo wa aciwembu udzadya ciwawa.
3Wogwira pakamwa pace asunga moyo wace;
Koma woyasamula milomo yace adzaonongeka.
4Moyo wa wolesi ukhumba osalandira kanthu;
Koma moyo wa akhama udzalemera.
5Wolungama ada mau onama;
Koma woipa anyansa, nadzicititsa manyazi,
6Cilungamo cicinjiriza woongoka m'njira;
Koma udio ugwetsa wocimwa.
7Alipo wodziyesa wolemera, koma alibe kanthu;
Alipo wodziyesa wosauka, koma ali ndi cuma cambiri.
8Ciombolo ca moyo wa munthu ndico cuma cace;
Koma wosauka samva cidzudzulo.
9Kuunika kwa olungama kukondwa;
Koma nyali ya oipa idzazima.
10Kudzikuza kupikisanitsa;
Koma omwe anauzidwa uphungu ali ndi nzeru.
11Cuma colandiridwa mokangaza cidzacepa;
Koma wokundika ndi dzanja adzaona zocuruka.
12Ciyembekezo cozengereza cidwalitsa mtima;
Koma pakufika cifuniroco ndico mtengo wa moyo.
13Wonyoza mau adziononga yekha;
Koma woopa malangizo adzalandira mphotho.
14Malamulo a wanzeru ndiwo kasupe wa moyo,
Apatutsa ku misampha ya imfa.
15Nzeru yabwino ipatsa cisomo;
Koma njira ya aciwembu iri makolokoto.
16Yense wocenjera amacita mwanzeru:
Koma wopusa aonetsa utsiru.
17Mthenga wolakwa umagwa m'zoipa;
Koma mtumiki wokhulupirika alamitsa.
18Wokana mwambo adzasauka nanyozedwa;
Koma wolabadira cidzudzulo adzalemekezedwa.
19Cifuniro cikondweretsa moyo citacitidwa;
Koma kusiya zoipa kunyansa opusa,
20Ukayenda ndi anzeru udzakhala wanzeru:
Koma mnzao wa opusa adzaphwetekedwa.
21Zoipa zilondola ocimwa;
Koma olungama adzalandira mphotho yabwino.
22Wabwino asiyira zidzukulu zace colowa cabwino;

Koma wocimwa angosungira wolungama cuma cace.
23M'kulima kwa osauka muli zakudya zambiri;
Koma zinazo zimaonongeka posowa ciweruzo.
24Wolekereramwanace osammenya amuda;
Koma womkonda amyambize kumlanga.
25Wolungama adya nakhutitsa moyo wace;
Koma mimba ya oipa idzasowa.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Miyambi 14
1Mkazi yense wanzeru amanga banja lace;
Koma wopusa alipasula ndi manja ace.
2Woyenda moongoka mtima aopa Yehova;
Koma wokhota m'njira yace amnyoza,
3M'kamwa mwa citsiru muli ntyole ya kudzikuza;
Koma milomo ya anzeru Idzawasunga.
4Popanda zoweta modyera muti see;
Koma mphamvu ya ng'ombe icurukitsa phindu.
5Mboni yokhulupirika sidzanama;
Koma mboni yonyenga imalankhula zonama.
6Wonyoza afunafuna nzeru osaipeza;
Koma wozindikira saona bvuto m'kuphunzira.
7Pita pamaso pa munthu wopusa,
Sudzazindikira milomo yakudziwa.
8Nzeru ya wocenjera ndiyo yakuti azindikire njira yace;
Koma utsiru wa opusa ndiwo cinyengo.
9Zitsiru zinyoza kuparamula;
Koma mwa oongoka mtima muli ciyanjano.
10Mtima udziwa kuwawa kwace kwace;
Mlendo sadudukira ndi cimwemwe cace.
11Nyumba ya oipa idzapasuka;
Koma hema wa oongoka mtima adzakula.
12Iripo njira yooneka kwa mwamuna ngati yoongoka;
Koma matsiriziro ace ndi njira za imfa.
13Ngakhale m'kuseka mtima uwawa;
Ndipo matsiriziro a ciphwete ndi cisoni.
14Wobwerera m'mbuyo m'mtima adzakhuta njira zace;
Koma munthu wabwino adzakhuta za mwa iye yekha.
15Wacibwana akhulupirira mau onse;
Koma wocenjera asamalira mayendedwe ace.
16Wanzeru amaopa nasiya zoipa;
Koma wopusa amanyada osatekeseka.
17Wokangaza kukwiya adzacita utsiru;
Ndipo munthu wa ziwembu adzadedwa.
18Acibwana amalandira colowa ca utsiru;
Koma ocenjera amabvala nzeru ngati korona.
19Oipa amagwadira abwino,
Ndi ocimwa pa makomo a olungama.
20Waumphawi adedwa ndi anzace omwe;
Koma akukonda wolemera acuruka.
21Wonyoza anzace acimwa;
Koma wocitira osauka cifundo adala.
22Kodi oganizira zoipa sasocera?

Koma akuganizira zabwino adzalandira cifundo ndi ntheradi.
23M'nchito zonse muli phindu;
Koma kulankhula-lankhula kungopatsa umphawi.
24Korona wa anzeru ndi cuma cao;
Utsiru wa opusa ndiwo utsiru.
25Mboni yoona imalanditsa miyoyo;
Koma wolankhula zonama angonyenga.
26Wakuopa Yehova akhulupirira kolimba;
Ndipo ana ace adzakhala ndi pothawirapo.
27Kuopa Yehova ndiko kasupe wa moyo,
Kupatutsa ku misampha ya imfa.
28Mu unyinji wa anthu muli ulemu wa mfumu;
Koma popanda anthu kalonga aonongeka.
29Wosakwiya msanga apambana kumvetsa;
Koma wansontho akuza utsiru.
30Mtima wabwino ndi moyo wa thupi;
Koma nsanje ibvunditsa mafupa.
31Wotsendereza aumphawi atonza Mlengi wace;
Koma wocitira wosauka cifundo amlemekeza.
32Wocimwa adzakankhidwa m'kuipa kwace;
Koma wolungama akhulupirirabe pomwalira,
33Nzeru ikhalabe m'mtima wa wozindikira,
Nidziwika pakati pa opusa.
34Cilungamo cikuza mtundu wa anthu;
Koma cimo licititsa pfuko manyazi.
35Mfumu ikomera mtima kapolo wocita mwanzeru;
Koma idzakwiyira wocititsa manyazi.

©The Bible Society of Malawi, 1992

1Mayankhidwe ofatsa abweza mkwiyo;
Koma mau owawitsa aputa msunamo.
2Lilime la anzeru linena bwino zomwe adziwa;
Koma m'kamwa mwa opusa mutsanulira utsiru.
3Maso a Yehova ali ponseponse,
Nayang'anira oipa ndi abwino.
4Kuciza lilime ndiko mtengo wa moyo;
Koma likakhota liswa moyo.
5Citsiru cipeputsa mwambo wa atate wace;
Koma wosamalira cidzudzulo amacenjera.
6M'nyumba ya wolungama muli katundu wambiri;
Koma m'phindu la woipa muli bvuto,
7Milomo ya anzeru iwanditsa nzeru,
Koma mtima wa opusa suli wolungama.
8Nsembe ya oipa inyansa Yehova;
Koma pemphero la oongoka mtima limkondweretsa.
9Njira ya oipa inyansa Yehova;
Koma akonda wolondola cilungamo.
10Wosiya njira adzalangidwa mowawa;
Wakuda cidzudzulo adzafa.
11Kumanda ndi kucionongeko kuli pamaso pa Yehova;
Koposa kotani nanga mitima ya ana a anthu?
12Wonyoza sakonda kudzudzulidwa,
Samapita kwa anzeru.
13Mtima wokondwa usekeretsa nkhope;
Koma moyo umasweka ndi zowawa za m'mtima.
14Mtima wa wozindikira ufunitsa kudziwa;
Koma m'kamwa mwa opusa mudya utsiru.
15Masiku onse a wosauka ali oipa;
Koma wokondwera mtima ali ndi phwando losatha.
16Zapang'ono, ulikuopa Yehova,
Zipambana ndi katundu wambiri pokhala phokoso,
17Kudya masamba, pali cikondano,
Kuposa ng'ombe yonenepa pali udani.
18Munthu wozaza aputa makani;
Koma wosakwiya msanga atonthoza makangano.
19Mayendedwe a wolesi akunga Hnga laminga,
Koma njira ya oongoka mtima iundidwa ngati mseu.
20Mwana wanzeru akondweretsa atate wace;
Koma munthu wopusa apeputsa amace.
21Wosowa nzeru akondwera ndi utsiru;
Koma munthu wozindikira aongola mayendedwe ace.
22Zolingalira zizimidwa popanda upo

Koma pocuruka aphungu zikhazikika.
23Munthu akondwera ndi mayankhidwe a m'kamwa mwace;
Ndi mau a pa nthawi yace kodi sali abwino?
24Anzeru ayesa njira yamoyo yokwerakwera,
Kuti apambuke kusiya kunsi kwa manda.
25Yehova adzapasula nyumba ya wonyada;
Koma adzalembera mkazi wamasiye malire ace,
26Ziwembu zoipa zinyansa Yehova;
Koma oyera mtima alankhula mau okondweretsa.
27Wopindula monyenga abvuta nyumba yace;
Koma wakuda mitulo adzakhala ndi moyo.
28Mtima wa wolungama uganizira za mayankhidwe;
Koma m'kamwa mwa ocimwa mutsanulira zoipa.
29Yehova atarikira oipa;
Koma pemphero la olungama alimvera.
30Kuunika kwa maso kukondweretsa mtima;
Ndipo pomveka zabwino mafupa amatenga uwisi.
31Khutu lomvera cidzudzulo ca moyo
Lidzakhalabe mwa anzeru.
32Wokana mwambo apeputsa moyo wace;
Koma wosamalira cidzudzulo amatenga nzeru.
33Kuopa Yehova ndiko mwambo wanzeru;
Ndipo cifatso citsogolera ulemu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

1Malongosoledwe a mtima nga munthu;
Koma mayankhidwe a lilime acokera kwa Yehova.
2Njira zonse za munthu ziyera pamaso pace;
Koma Yehova ayesa mizimu.
3Pereka zocita zako kwa Yehova,
Ndipo zolingalira zako zidzakhazikika.
4Zonse Yehova anazipangaziri ndi zifukwa zao;
Ngakhale amphulupulu kuti aone tsiku loipa,
5Yense wonyada mtima anyansa Yehova;
Zoonadi sadzapulumuka cilango.
6Mphulupulu iomboledwa ndi cifundo ndi ntheradi;
Apatuka pa zoipa poopa Yehova.
7Njira za munthu zikakonda Yehova,
Ayanjanitsana naye ngakhale adani ace.
8Zapang'ono, pokhala cilungamo,
Ziposa phindu lalikuru lopanda ciweruzo.
9Mtima wa munthu ulingalira njira yace;
Koma Yehova ayendetsa mapazi ace.
10Mau a mlauli ali m'milomo ya mfumu;
M'kamwa mwace simudzacita cetera poweruza.
11Mwini muyeso ndi mulingo wolungama ndiye Yehova;
Ndiyenso anapanga miyala yonse yoyesera ya m'thumba.
12Kucita mphulupulu kunyansa mafumu;
Pakuti mpando wao wakhazikika ndi cilungamo.
13Milomo yolungama ikondweretsa mafumu;
Wonena zoongoka amkonda.
14Mkwiyo wa mfumu ndi mithenga ya imfa;
Wanzeru adzaukhulula.
15M'kuunika kwa nkhope ya mfumu muli moyo;
Kukoma mtima kwace kunga mtambo wa mvula ya masika.
16Kodi kulandira nzeru sikupambana ndi golidi,
Kulandira luntha ndi kusankhika koposa siliva?
17Khwalala la oongoka mtima ndilo lakuti asiye zoipa;
Wosunga njira yace acinjiriza moyo wace.
18Kunyada kutsogolera kuonongeka
Mtinia wodzikuza ndi kutsogolera kupunthwa.
19Kufatsa mtima ndi osauka
Kuposa kugawana zofunkha ndi onyada.
20Wolabadira mau adzapeza bwino;
Ndipo wokhulupirira Yehova adala.
21Wanzeru mtima adzachedwa wocenjera;
Ndipo kukoma kwa milomo kuyenjezera kuphunzira.
22Nzeru ndi kasupe wa moyo kwa mwini wace;

Koma mwambo wa zitsiru ndi utsiru.
23Mtima wa wanzeru ucenjeza m'kamwa mwace,
Nuphunzitsanso milomo yace.
24Mau okoma ndiwo cisa ca uci,
Otsekemera m'moyo ndi olamitsa mafupa.
25Iripo njira yooneka kwa mwamuna ngati yoongoka,
Koma matsiriziro ace ndi njira za imfa.
26Wanchito adzigwirira yekha nchito;
Pakuti m'kamwa mwace mumfulumiza.
27Munthu wopanda pace akonzeratu zoipa;
Ndipo m'milomo mwace muli moto wopsereza.
28Munthu wokhota amautsa makani;
Kazitape afetsa ubwenzi.
29Munthu waciwawa akopa mnzace,
Namuyendetsa m'njira yosakhala bwino.
30Wotsinzina ndiye aganizira zakhota;
Wosunama afikitsa zoipa.
31Imvi ndiyo korona wa ulemu,
Idzapezedwa m'njira ya cilungamo.
32Wosakwiya msanga aposa wamphamvu;
Wolamulira mtima wace naposa wolanda mudzi.
33Maere aponyedwa pamfunga;
Koma ndiye Yehova alongosola zonse.

©The Bible Society of Malawi, 1992

1Nyenyeswa youma, pokhala mtendere,
Iposa nyumba yodzala nyama yansembe, pali makangano.
2Kapolo wocitamwanzeru
Adzalamulira mwana wocititsa manyazi,
Nadzagawana nao abale colowa.
3Siliva ali ndi mbiya yosungunulira, golidi ali ndi ng'anjo;
Koma Yehova ayesa mitima.
4Wocimwa amasamalira milomo yolakwa;
Wonama amvera lilime losakaza.
5Wocitira ciphwete aumphawi atonza Mlengi;
Wokondwera ndi tsoka sadzapulumuka cilango.
6Zidzukulu ndizo korona wa okalamba;
Ndipo ulemerero wa ana ndiwo atate ao.
7Mlomo wangwiro suyenera citsiru;
Ngakhale mlomo wonama suyenera kalonga ndi pang'ono ponse.
8Wolandira cokometsera mlandu aciyesa ngale;
Pali ponse popita iye acenjera.
9Wobisa colakwa afunitsa cikondano;
Koma wobwereza-bwereza mau afetsa ubwenzi.
10Cidzudzulo cilowa m'kati mwa wozindikira,
Kopambana ndi kukwapula wopusa kwambiri.
11Woipa amafuna kupanduka kokha;
Koma adzamtumizira mthenga wankhanza.
12Kukomana ndi citsiru m'kupusa kwace
Kuopsya koposa cirombo cocicotsera anace.
13Wobwezera zabwino zoipa,
Zoipa sizidzamcokera kwao.
14Ciyambi ca ndeu cifanana ndi kutsegulira madzi;
Tsono kupikisana kusanayambe tasiya makani.
15Wokometsa mlandu wa wamphulupulu, ndi wotsutsa wolungama,
Onse awiriwa amnyansa Yehova.
16Kodi bwanji mtengo wogulira nzeru uli m'dzanja la citsiru,
Popeza wopusa alibe mtima?
17Bwenzi limakonda nthawi zonse;
Ndipo mbale anabadwira kuti akuthandize pooneka tsoka.
18Munthu wosowa nzeru apangana kulipirira wina,
Napereka cikole pamaso pa mnzace.
19Wokonda ndeu akonda kulakwa;
Ndipo wotarikitsa khomo lace afunafuna kuonongeka.
20Wokhota mtima sadzapeza bwino
Ndipo mwini lilime lokhota adzagwa m'zoipa.
21Wobala citsiru adzicititsa cisoni;
Ndipo atate wa wopusa sakondwa.

22Mtima wosekerera uciritsa bwino
Koma mzimu wosweka uphwetsa mafupa,
23Munthu woipa alandira cokometsera mlandu coturutsa m'mfunga,
Kuti apambukitse mayendedwe a ciweruzo.
24Nzeru iri pamaso pa wozindikira;
Koma maso a wopusa ali m'malekezero a dziko.
25Mwana wopusa acititsa atate wace cisoni,
Namvetsa zowawa amace wombala.
26Kulipiritsa wolungama sikuli kwabwino,
Ngakhale kukwapula akuru cifukwa aongoka mtima.
27Wopanda cikamwakamwa apambana kudziwa;
Ndipo wofatsa mtima ali wanzeru.
28Ngakhalecitsirucikatontholaaciyesa canzeru;
Posunama ali wocenjera.

©The Bible Society of Malawi, 1992

1Wopanduka afunafuna niro cace,
Nakangana ndi nzeru yonse yeniyeni.
2Wopusa sakondwera ndi kuzindikira;
Koma kungobvumbulutsa za m'mtima mwace.
3Pakudza wamphulupulu padzanso kunyoza;
Manyazi natsagana ndi citonzo.
4Mau a m'kamwa mwa munthu ndiwo madzi akuya;
Kasupe wa nzeru ndiye mtsinje wodzala.
5Kukometsa mlandu wa wamphulupulu mwatsankhu sikuli kwabwino,
Ngakhale kucitira cetera wolungama.
6Milomo ya wopusa ifikitsa makangano;
Ndipo m'kamwa mwace muputa kukwapulidwa.
7M'kamwa mwa wopusa mumuononga,
Milomo yace ikhala msampha wa moyo wace.
8Mau a kazitape akunga zakudya zolongosoka,
Zotsikira m'kati mwa mimba.
9Wogwira nchito mwaulesi
Ndiye mbale wace wa wosakaza.
10Dzina la Yehova ndilo linga lolimba;
Wolungama athamangiramo napulumuka.
11Cuma ca wolemera ndico mudzi wace wolimba;
Alingalira kuti ndico khoma lalitari.
12Mtima wa munthu unyada asanaonongeke;
Koma cifatso citsogolera ulemu.
13Wobwezera mau asanamvetse apusa,
Nadzicititsa manyazi.
14Mtima wa munthu umlimbitsa alikudwala;
Koma ndani angatukule mtima wosweka?
15Mtima wa wozindikira umaphunzira;
Khutu la anzeru lifunitsa kudziwa.
16Mtulo wa munthu umtsegulira njira,
Numfikitsa pamaso pa akuru.
17Woyamba kudzinenera ayang'anika wolungama;
Koma mnzace afika namuululitsa zace zonse.
18Ula uletsa makangano,
Nulekanitsa amphamvu.
19Kupembedza mbale utamcimwira nkobvuta,
Kulanda mudzi wolimba nkosabvuta;
Makangano akunga mipiringidzo ya linga.
20Mimba ya munthu idzakhuta zipatso za m'kamwa mwace;
Iye nadzakhuta phindu la milomo yace.
21Lilime liri ndi mphamvu pa imfa ndi moyo;

Wolikonda adzadya zipatso zace.
22Wopeza mkazi apeza cinthu cabwino;
Yehova amkomera mtima.
23Wosauka amadandaulira;
Koma wolemera ayankha mwaukali.
24Woyanjana ndi ambiri angodziononga;
Koma liripo bwenzi lipambana ndi mbale kuumirira.

©The Bible Society of Malawi, 1992

1Wosauka woyenda mwangwiro
Aposa wokhetsa milomo ndi wopusa.
2Kukhumba kosadziwa sikuli kwabwino;
Ndipo wofulumira ndi mapazi ace amacimwa.
3Utsiru wa munthu ukhotetsa njira yace;
Mtima wace udandaula pa Yehova.
4Cuma cionjezetsa mabwenzi ambiri;
Koma mnzace wa waumphawi amleka.
5Mboni yonama sidzakhala yosalangidwa;
Wolankhula mabodza sadzapulumuka.
6Ambiri adzapembedza waufulu;
Ndipo yense ndi bwenzi la munthu wopatsa.
7Abale onse a wosauka amuda;
Nanga mabwenzi ace kodi satanimphirana naye?
Awatsata ndi mau, koma kuli zi.
8Wolandira nzeru akonda moyo wace;
Wosunga luntha adzapeza zabwino.
9Mboni yonama sidzapulumuka cilango;
Wolankhula mabodza adzaonongeka.
10Wopusa sayenera kukhala ndi zinthu zolongosoka;
Nanga kapolo ayenera kulamulira akalonga kodi?
11Kulingalira kwa munthu kucedwetsa mkwiyo;
Ulemerero wace uli wakuti akhululukire colakwa.
12Mkwiyo wa mfumu ukunga kubangula kwa mkango;
Koma kukoma mtima kwace kunga mame pamsipu.
13Mwana wopusa ndiye tsoka la atate wace;
Ndipo makangano a mkazi ndiwo kudontha-donthabe.
14Nyumba ndi cuma ndizo colowa ca atate;
Koma mkazi wanzeru acokera kwa Yehova.
15Ulesi ugonetsa tulo tofa nato;
Ndipo moyo wamkhongono udzamva njala.
16Wosunga lamulo asunga moyo wace;
Wonyalanyaza mayendedwe ace adzafa.
17Wocitira waumphawi cifundo abwereka Yehova;
Adzambwezera cokoma caceco.
18Menya mwanako, ciyembekezero ciripo,
Osafunitsa kumuononga.
19Munthu waukali alipire mwini;
Pakuti ukampulumutsa udzateronso.
20Tamvera uphungu, nulandire mwambo,
Kuti ukhale wanzeru pa cimariziro cako,
21Muli zolingalira zambiri m'mtima mwa munthu;
Koma uphungu wa Yehova ndiwo udzaimika.

22Cotikondetsa munthu ndico kukoma mtima kwace;
Ndipo wosauka apambana munthu wonama.
23Kuopa Yehova kupatsa moyo;
Wokhala nako adzakhala wokhuta;
Zoipa sizidzamgwera.
24Wolesi alonga dzanja lace m'mbale,
Osalibwezanso kukamwa kwace.
25Menya wonyoza, ndipo acibwana adzaceniera;
Nudzudzule wozindikira adzazindikira nzeru.
26Wolanda za atate, ndi wopitikitsa amai,
Ndiye mwana wocititsa manyazi ndi wogwetsa nkhope.
27Ukangofuna, mwananga, kusocera kusiya mau akudziwitsa,
Leka kumva mwambo.
28Mboni yopanda pace inyoza ciweruzo;
M'kamwa mwa amphulupulu mumeza zoipa,
29Akonzera onyoza ciweruzo,
Ndi mikwingwirima pamsana pa opusa.

©The Bible Society of Malawi, 1992

1Vinyo acita ciphwete, cakumwa caukali cisokosa;
Wosocera nazo alibe nzeru.
2Kuopsya kwa mfumu ndiko kubangula kwa mkango;
Womputa acimwira moyo wace wace.
3Kuli ulemu kwa mwamuna kupewa ndeu;
Koma zitsiru zonse zimangokangana,
4Wolesi salima cifukwa ca cisanu;
Adzapemphapempha m'masika osalandira kanthu.
5Uphungu wa m'mtima mwa munthu ndiwo madzi akuya;
Koma munthu wozindikira adzatungapo,
6Anthu ambiri abukitsa yense kukoma mtima kwace;
Koma ndani angapeze munthu wokhulupirika?
7Wolungama woyenda mwangwiro,
Anace adala pambuyo pace.
8Mfumu yokhala pa mpando waweruzira
Ipitikitsa zoipa zonse ndi maso ace.
9Ndani anganene, Ndasambitsa mtima wanga,
Ndayera opanda cimo?
10Miyeso yosiyana, ndi malicero osiyana,
Zonse ziwirizi zinyansa Yehova.
11Ngakhale mwana adziwika ndi nchito zace;
Ngati nchito yace iri yoyera ngakhale yolungama.
12Khutu lakumva, ndi diso lopenya,
Yehova anapanga onse awiriwo.
13Usakonde tulo ungasauke;
Phenyula maso, udzakhuta zakudya.
14Wogula ati, Cacabe cimeneco.
Koma atacoka adzitama.
15Alipo golidi ndi ngale zambiri;
Koma milomo yodziwa ndiyo cokometsera ca mtengo wapatari.
16Tenga maraya a woperekera mlendo cikole;
Woperekera mkazi wacilendo cikole umgwire mwini.
17Zakudya za cinyengo zikondweretsa munthu;
Koma pambuyo pace m'kamwa mwace mudzadzala tinsangalabwi.
18Uphungu utsimikiza zolingalira,
Ponya nkhondo utapanga upo.
19Kazitape woyendayenda awanditsa zinsinsi;
Usadudukire woyasama milomo yace.
20Wotemberera atate wace ndi, amace,
Nyali yace idzazima mu mdima woti bi.
21Colowa cingalandiridwe msanga msanga poyamba pace;
Koma citsiriziro cace sicidzadala.
22Usanene, Ndidzabwezera zoipa;

Yembekeza Yehova, adzakupulumutsa.
23Miyeso yosiyana inyansa Yehova,
Ndi mulingo wonyenga suli wabwino.
24Yehova alongosola mayendedwe a mwamuna;
Munthu tsono angazindikire bwanji njira yace?
25Kunena mwansontho, ici ncopatulika, kuli msampha kwa munthu,
Ndi kusinkhasinkha pambuyo pace atawinda.
26Mfumu yanzeru ipeta amphulupulu,
Niyendetsapo njinga ya gareta.
27Mzimu wa munthu ndiwo nyali ya Yehova;
Usanthula m'kati monse mwa mimba.
28Cifundo ndi ntheradi zisunga mfumu;
Cifundo cicirikiza mpando wace.
29Ulemerero wa anyamata ndiwo mphamvu yao;
Kukongola kwa nkhalamba ndi
30Mikwingwirima yopweteka icotsa zoipa;
Ndi mikwapulo ilowa m'kati mwa mimba.

©The Bible Society of Malawi, 1992

1Mtima wa mfumu uli m'dzanja la Yehova ngati mitsinje ya madzi;
Aulozetsa komwe afuna.
2Njira zonse za munthu zilungama pamaso pace;
Koma Yehova ayesa mitima.
3Kucita cilungamo ndi ciweruzo
Kupambana ndi nsembe kumkonda Yehova.
4Maso akunyada, ndi mtima wodzikuza,
Ndi nyali ya oipa, ziri cimo.
5Zoganizira za wakhama zicurukitsadi katundu;
Koma yense wansontho angopeza umphawi.
6Kupata cuma ndi lilime lonama ndiko nkhungu yoyendayenda,
ngakhale misampha ya imfa.
7Ciwawa ca amphulupulu cidzawakokolola;
Cifukwa akana kucita ciweruzo.
8Wosenza cimo njira yace ikhotakhota;
Koma nchito ya woyera mtima ilungama.
9Kukhala pa ngondya ya tsindwi kufunika
Kuposa kukhala m'nyumba ndi mkazi wolongolola.
10Wamphulupulu mtima wace umkhumba zoipa;
Sakomera mtima mnzace.
11Polangidwa wonyoza, wacibwana alandira nzeru,
Naphunzira pakuyang'ana pa wanzeru.
12Wolungama aganizira za nyumba ya wamphulupulu,
Kuti amphulupulu amagwetsedwa, naona zoipa.
13Wotseka makutu ace polira waumphawi,
Nayenso adzalira koma osamvedwa.
14Mphatso ya m'tseri ipembedza mkwiyo,
Ndi mtulo wa pamfunga ukali wolimba.
15Kucita ciweruzo kukondweretsa wolungama;
Koma kuwaononga akucita mphulupulu,
16Munthu wosocera pa njira ya nzeru
Adzakhala m'msonkhano wa akufa.
17Wokonda zoseketsa adzasauka;
Wokonda vinyo ndi mafuta sadzalemera.
18Wocimwa ndiye ciombolo ca wolungama;
Ndipo waciwembu adzalowa m'malo mwa oongoka mtima.
19Kukhala m'cipululu kufunika
Kuposa kukhala ndi mkazi wolongolola ndi wong'ung'udza.
20Mokhala wanzeru muli katundu wofunika ndi mafuta;
Koma wopusa angozimeza.
21Wolondola cilungamo ndi cifundo
Apeza moyo, ndi cilungamo, ndi ulemu.
22Wanzeru akwera pa mudzi wa olimba,

Nagwetsa mphamvu yace imene anaikhulupirira.
23Wosunga m'kamwa mwace ndi lilime lace
Asunga moyo wace kumabvuto.
24Wonyada wodzikuza dzina lace ndiye wonyoza;
Acita mwaukali modzitama.
25Cifuniro ca wolesi cimupha;
Cifukwa manja ace akana kugwira nchito.
26Ena asirira modukidwa tsiku lonse;
Koma wolungama amapatsa osamana.
27Nsembe ya oipa inyansa;
Makamaka pakudza nayo iwo mwaciwembu.
28Mboni yonama idzafa;
Koma mwamuna wakumvetsa adzanena mosakayika,
29Munthu woipa aumitsa nkhope yace;
Koma woongoka mtima akonza njira zace.
30Kulibe nzeru ngakhale luntha
Ngakhale uphungu wotsutsana ndi Yehova.
31Kavalo amakonzedweratu cifukwa ca tsiku la nkhondo;
Koma wopulumutsa ndiye Yehova.

©The Bible Society of Malawi, 1992

1Mbiri yabwino ifunika kopambana cuma cambiri;
Kukukomera mtima anzako kuposa siliva ndi golidi.
2Wolemera ndi wosauka akumana,
Wolenga onsewo ndiye Yehova.
3Wocenjera aona zoipa, nabisala;
Koma acibwana angopitirira, nalipitsidwa.
4Mphotho ya cifatso ndi kuopa, Yehova
Ndiye cuma, ndi ulemu, ndi moyo.
5Minga ndi misampha iri m'njira ya wokhota;
Koma wosunga moyo wace adzatarikira imeneyo.
6Phunzitsa mwana poyamba njira yace;
Ndipo angakhale atakalamba sadzacokamo.
7Wolemera alamulira osauka;
Ndipo wokongola ndiye kapolo wa womkongoletsa.
8Wofesa zosalungama adzakolola tsoka;
Ndipo ntyole ya mkwiyo wace idzalephera.
9Mwini diso lamataya adzadala;
Pakuti apatsa osauka zakudya zace.
10Ukainga wonyoza, makangano adzaturuka;
Makani ndi manyazi adzalekeka.
11Wokonda kuyera mtima,
Mfumu idzakhala bwenzi lace cifukwa ca cisomo ca milomo yace.
12Maso a Yehova acinjiriza wodziwa;
Koma agwetsa mau a munthu wa ziwembu.
13Waulesi ati, Pali mkango panjapo,
Ndidzaphedwa pamakwalalapo.
14M'kamwa mwa mkazi waciwerewere muli dzenje lakuya;
Yemwe Yehova amkwiyira adzagwamo.
15Utsiru umangidwa mumtima mwa mwana;
Koma ntyole yomlangira idzauingitsira kutari.
16Wotsendereza waumphawi kuti acurukitse cuma cace,
Ndi wopatsa wolemera kanthu, angosauka.
Malangizo a pa makhalidwe oyenera munthu
17Chera makutu ako, numvere mau a anzeru,
Nulozetse mtima wako kukadziwa zanga.
18Pakuti mauwo akondweretsa ngati uwasunga m'kati mwako,
Ngati akhazikika pamodzi pa milomo yako.
19Ndakudziwitsa amenewo lero, ngakhale iwedi,
Kuti ukhulupirire Yehova.
20Kodi sindinakulembera zoposa Za uphungu ndi nzeru;
21Kuti ukadziwitse ntheradi yace ya mau oona,
Nukabwere ndi mau oona kwa iwo amene anakutumiza?
22Usalande za waumphawi cifukwa ali waumphawi,

Ngakhale kutsendereza wosauka kubwalo.
23Pakuti Yehova adzanenera mlandu wao;
Omwe akwatula zao Iye adzakwatula moyo wao.
24Usayanjane ndi munthu wokwiya msanga;
Ngakhale kupita ndi mwamuna waukali;
25Kuti ungaphunzire mayendedwe ace,
Ndi kutengera moyo wako msampha,
26Usakhale wodulirana mpherere,
Ngakhale kumperekera cikole ca ngongole zace.
27Ngati ulibe cobwezera
Kodi acotserenji kama lako pansi pako?
28Usasunthe cidziwitso cakale ca m'malire,
Cimene makolo ako anaciimika.
29Kodi upenya munthu wofulumiza nchito zace?
Adzaima pamaso pa mafumu, osaima pamaso pa anthu acabe.

©The Bible Society of Malawi, 1992

1Pamene ukhala ulinkudya ndi mkuru,
Zikumbukira ameneyo ali pamaso pako;
2Nuike mpeni pakhosi pako,
Ngati uli wadyera.
3Usakhumbe zolongosoka zace;
Pokhala zakudya zonyenga.
4Usadzitopetse kuti ulemere;
Leka nzeru yako yako.
5Kodi upenyeranji cimene kulibe?
Pakuti cuma cunera mapiko,
Ngati mphungu youluka mumlengalenga.
6Usadye zakudya zace za wa maso ankhwenzule,
Ngakhale kukhumba zolongosoka zace;
7Pakuti monga asinkha m'kati mwace, ali wotere;
Ati kwa iwe, Idya numwe;
Koma mtima wace suli pa iwe.
8Pakuti nthongo imene unaidya udzaisanza,
Ndi kutaya mau ako okondweretsa.
9Usalankhule m'makutu a wopusa;
Pakuti adzapeputsa nzeru ya mau ako.
10Usasunthe cidziwitso cakale ca m'malire;
Ngakhale kulowa m'minda ya amasiye;
11Pakuti Mombolo wao walimba;
Adzawanenera mlandu wao pa iwe.
12Lozetsa mtima wako kumwambo,
Ndi makutu ako ku mau a nzeru.
13Usamane mwana cilango;
Pakuti ukammenya ndi ntyole safa ai.
14Udzammenya ndi ntyole,
Nudzapulumutsa moyo wace kunsi kwa manda.
15Mwananga, mtima wako ukakhala wanzeru,
Mtima wanga wa inedi udzakondwa;
16Imso zanga zidzasangalala,
Polankhula milomo yako zoongoka.
17Mtima wako usacitire nsanje akucimwawo;
Koma opabe Yehova tsiku lonse;
18Pakutitu padzakhala mphotho;
Ndipo ciyembekezo cako sicidzalephereka.
19Tamvera tsopano, mwananga, utenge nzeru,
Ulunjikitse mtima wako m'njiramo.
20Usakhale mwa akumwaimwa vinyo,
Ndi ankhuli osusuka.
21Pakuti wakumwaimwa ndi wosusukayo adzasauka;

Ndipo kusinza kudzabveka munthu nsanza.
22Tamvera atate wako anakubala,
Usapeputse amako atakalamba.
23Gula ntheradi, osaigulitsa;
Nzeru, ndi mwambo, ndi luntha.
24Atate wa wolungama adzasekeradi;
Wobala mwana wanzeru adzakondwera naye.
25Atate wako ndi amako akondwere,
Amako wakukubala asekere.
26Mwananga, undipatse mtima wako,
Maso ako akondwere ndi njira zanga,
27Pakuti mkazi wadama ndiye dzenje lakuya;
Ndipo mkazi waciwerewere ndiye mbuna yopapatiza.
28Pakuti abisalira ngati wacifwamba,
Nacurukitsa anthu a ciwembu.
29Ndani ali ndi cisoni? ndani asauka? ndani ali ndi makangano?
Ndani ang'ung'udza? ndani alasidwa cabe? ndani afiira maso?
30Ngamene acedwa pali vinyo,
Napita kukafunafuna vinyo wosanganizidwa.
31Usayang'ane pavinyo alikufiira.
Alikung'azimira m'cikho.
Namweka mosalala.
32Pa citsiriziro cace aluma ngati njoka,
Najompha ngati mamba.
33Maso ako adzaona zacilendo,
Mtima wako udzalankhula zokhota.
34Udzafanana ndi wina wogona pakati pa nyanja,
Pena wogona pa nsonga ya mlongoti wa ngalawa.
35Udzati, Anandimenya, osaphwetekedwa ine;
Anandikwapula, osamva ine;
Ndidzauka nthawi yanji? Ndidzafuna-funanso vinyoyo.

©The Bible Society of Malawi, 1992

1Usacitire nsanje anthu oipa, Ngakhale kufuna kukhala nao;
2Pakuti mtima wao ulingalira za cionongeko;
Milomo yao ilankhula za mphulupulu.
3Nzeru imangitsa nyumba;
Luntha liikhazikitsa.
4Kudziwa kudzaza zipinda zace
Ndi cuma conse cofunika ca mtengo wace.
5Mwamuna wanzeru ngwamphamvu;
Munthu wodziwa ankabe nalimba.
6Pakuti udzaponya nkhondo yako ndi upo,
Ndi kupulumuka pocuruka aphungu,
7Nzeru itarikira citsiru;
Satsegula pakamwa kubwalo.
8Wolingalira zakucita zoipa
Anthu adzamcha waciwembu.
9Maganizo opusa ndiwo cimo;
Wonyoza anyansa anthu.
10Ukalefuka tsiku la tsoka
Mphamvu yako icepa.
11Omwe atengedwa kuti akafe, uwapulumutse;
Omwe ati aphedwe, usaleke kuwalanditsa.
12Ukanena, Taonani, sitinadziwa cimeneci;
Kodi woyesa mitima sacizindikira ici?
Ndi wosunga moyo wako kodi sacidziwa?
Ndipo kodi sabwezera munthu yense monga mwa macitidwe ace?
13Mwananga, idya uci pakuti ngwabwino,
Ndi cisa cace citsekemera m'kamwamwako;
14Potero udzadziwa kuti nzeru iri yotero m'moyo wako;
Ngati waipeza padzakhala mphotho,
Ndipo ciyembekezo cako sicidzalephereka.
15Usabisalire, woipa iwe, pomanga wolungama;
Usapasule popuma iyepo.
16Pakuti wolungama amagwa kasanu ndi kawiri, nanyamukanso;
Koma oipa akhumudwa pomfikira tsoka.
17Usakondwere pakugwa mdani wako;
Mtima wako usasekere pokhumudwa iye;
18Kuti Yehova angaone kukondwa kwako, ndi kukuyesa koipa,
Ndi kuleka kumkwiyira.
19Usabvutike mtima cifukwa ca ocita zoipa;
Ngakhale kucitira nsanje amphulupulu;
20Pakuti woipayo sadzalandira mphotho;
Nyali ya amphulupulu idzazima.
21Mwananga, opa Yehova ndi mfumu yomwe,

Osadudukira anthu osinthasintha.
22Pakuti tsoka lao lidzaoneka modzidzimuka;
Ndipo ndani adziwa cionongeko ca zaka zao?
23Izinso ziri za anzeru.
Poweruza cetera siliri labwino.
24Wonenakwa woipa, Wolungama iwe;
Magulu a anthu adzamtemberera, mitundu ya anthu idzamkwiyira,
25Omwe amdzudzula adzasekera,
Nadzadalitsika ndithu.
26Wobwezera mau oongoka
Apsompsona milomo.
27Longosola nchito yako panjapo, nuikonzeretu kumunda;
Pambuyo pace ndi kumanga nyumba yako.
28Usacitire mnzako umboni womtsutsa opanda cifukwa;
Kodi udzanyenga ndi milomo yako?
29Usanene, Ndidzamcitira zomwezo anandicitira ine;
Ndidzabwereza munthuyo monga mwa macitidwe ace.
30Ndinapita pa munda wa wolesi,
Polima mphesa munthu wosowa nzeru.
31Taonani, ponsepo panamera minga,
Ndi kuwirirapo khwisa;
Chinga lace lamiyala ndi kupasuka.
32Pamenepo ndinayang'ana ndi kuganizira,
Ndinaona ndi kulandira mwambo.
33Tulo tapang'ono, kungoodzera pang'ono,
Kungomanga manja pang'ono m'kugona,
34Ndipo umphawi wako udzafika ngati mbala;
Ndi kusauka kwako ngati munthu wacikopa.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Miyambo ya Solomo yosonkhanitsa nthawi ya Hezekiya

1Iyinso ndiyo miyambo ya Solomo
Imene anthu a Hezekiya mfumu ya Yuda anailemba.
2Kubisa kanthu ndi ulemerero wa Mulungu;
Koma ulemerero wa mafumu ndi kusanthula kanthu.
3Pamlengalenga patarika, ndi padziko pakuya,
Koma mitima ya mafumu singasanthulike.
4Cotsera siliva mphala yace,
Mmisiri wa ng'anjo aturutsamo mbale;
5Cotsera woipa pamaso pa mfumu,
Mpando wace udzakhazikika m'cilungamo.
6Usadzitame pamaso pa mfumu,
Ngakhale kuima m'malo mwa akuru;
7Pakuti kunena kwa iwe, Takwera kuno,
Kupambana ndi kuti utsitsidwe pamaso pa kalonga,
Amene maso ako anamuona.
8Usaturuke mwansontho kukalimbana,
Ungalephere pa kutha kwace,
Atakucititsa mnzako manyazi.
9Nena mlandu wako ndi mnzako,
Osaulula zinsinsi za mwini;
10Kuti wakumva angakutonze,
Mbiri yako yoipa ndi kusacoka.
11Mau oyenera a pa nthawi yace
Akunga zipatso zagolidi m'nsengwa zasiliva.
12Monga phelele lagolidi ndi cipini cagolidi woyengeka,
Momwemo wanzeru wodzudzula pa khutu lomvera.
13Monga cisanu ca cipale cofewa pa nthawi ya masika,
Momwemo mthenga wokhulupirika kwa amene anamtuma;
Atsitsimutsa moyo wa ambuyace.
14Monga mitambo ndi mphepo popanda mvula,
Momwemo ndiye wodzikweza ndi zipatso zace monyenga.
15Cipiriro cipembedza mkuru;
Lilime lofatsa lityola pfupa,
16Wapeza uci kodi? Idyapo wokwanira,
Kuti ungakukole, nusanze.
17Phazi lako lilowe m'nyumba ya mnzako kamodzi kamodzi;
Kuti angatope nawe ndi kukuda.
18Wocitira mnzace umboni wonama
Ndiye cibonga, ndi lupanga, ndi mubvi wakuthwa.
19Kukhulupirira munthu wa ciwembu tsiku latsoka
Kunga dzino lotyoka ndi phazi loguluka.
20Monga wobvula maraya tsiku lamphepo,

Ngakhale kuthira vinyo wosasa m'soda,
Momwemo woyimbira nyimbo munthu wacisoni.
21Mdani wako akamva njala umdyetse,
Akamva ludzu ummwetse madzi,
22Pakuti udzaunjika makala amoto pamtu pace;
Ndipo Yehova adzakupatsa mphotho,
23Mphepo ya kumpoto ifikitsa mvula;
Comweco lilime losinjirira likwiyitsa nkhope.
24Kukhala pa ngondya ya tsindwi kufunika
Kuposa kukhala m'nyumba ndi mkazi wolongolola.
25Monga madzi ozizira kwa munthu wotopa,
Momwemo mau abwino akucokera ku dziko lakutari.
26Monga kasupe wopondedwa, ndi citsime cobvonongeka,
Momwemo wolungama ngati akonjera woipa.
27Kudya uci wambiri sikuli kwabwino;
Comweco kufunafuna ulemu wako wako sikuli ulemu.
28Wosalamulira mtima wace
Akunga mudzi wopasuka wopanda linga,

©The Bible Society of Malawi, 1992

1Monga cipale cofewa m'malimwe, ndi mvula m'masika,
Momwemo ulemu suyenera citsiru.
2Monga mpheta irikuzungulira, ndi namzeze alikuuluka,
Momwemo temberero la pacabe silifikira.
3Cikoti ciyenera kavalo, ndi cam'kamwa ciyenera buru,
Ndi ntyole iyenera pamsana pa zitsiru.
4Usayankhe citsiru monga mwa utsiru wace,
Kuti ungafanane naco iwe wekha.
5Yankha citsiru monga mwa utsiru wace,
Kuti asadziyese wanzeru.
6Wotumiza mau ndi dzanja la citsiru
Adula mapazi ace, namwa zompweteka.
7Miyendo ya wopunduka iri yolobodoka,
Momwemo mwambi m'kamwa mwa zitsiru.
8Monga thumba la ngale m'mulu wa miyala,
Momwemo wocitira citsiru ulemu.
9Monga munga wolasa dzanja la woledzera,
Momwemo mwambi m'kamwa mwa zitsiru.
10Monga woponya mibvi ndi kulasa onse,
Momwemo wolembera citsiru, ndi wolembera omwe alikupita panjira.
11Monga garu abweranso ku masanzi ace,
Momwemo citsiru cicitanso zopusa zace.
12Kodi uona munthu wodziyesa wanzeru?
Ngakhale citsiru cidzacenjera koma ameneyo ai.
13Wolesi ati, Mkango uli panjira,
Wobangulawo uli m'makwalala.
14Monga citseko cikankhikira pa zitsulo za pamphuthu,
Momwemo wolesi agubuduka pakama pace.
15Wolesi alonga dzanja lace m'mbale;
Kumtopetsa kulibweza kukamwa kwace.
16Wolesi adziyesa wanzeru
Koposa anthu asanu ndi awiri akuyankha mozindikira.
17Wakungopita ndi kubvutika ndi ndeu yosakhala yace
Akunga wogwira makutu a garu.
18Monga woyaruka woponya nsakali,
Mibvi, ndi imfa,
19Momwemo wonyenga mnzace ndi kuti, Ndi kusewera kumeneku.
20Posowa nkhuni moto ungozima;
Ndi popanda kazitape makangano angoleka.
21Monga makala ozizira pa makala akunyeka, ndi nkhuni pamoto;
Momwemo munthu wamakangano autsa ndeu.
22Mau a kazitape ndi zakudya zolongosoka

Zitsikira m'kati mwa mimba.
23Milomo yofunitsitsa ndi mtima woipa
Ikunga mbale yadothi anaimata ndi mphala yasiliva.
24Wakuda mnzace amanyenga ndi milomo yace;
Koma akundika cinyengo m'kati mwace;
25Pamene akometsa mau ace usamkhulupirire;
Pakuti m'mtima mwace muli zonyansa zisanu ndi ziwiri.
26Angakhale abisa udani wace pocenjera,
Koma udio wace udzabvumbulutsidwa posonkhana anthu.
27Wokumba dzenje adzagwamo,
Wogubuduza mwala, udzabweranso pa iye mwini.
28Lilime lonama lida omwewo linawasautsa;
Ndipo m'kamwa mosyasyalika mungoononga.

©The Bible Society of Malawi, 1992

1Usanyadire zamawa,
Popeza sudziwa tsiku lina lidzabala ciani?
2Wina akutame, si m'kamwamwako ai;
Mlendo, si milomo ya iwe wekha.
3Mwala ulemera, mcenga ndiwo katundu;
Koma mkwiyo wa citsiru upambana kulemera kwace.
4Kupweteka mtima nkwa nkhanza, mkwiyo usefuka;
Koma ndani angalakike ndi nsanje?
5Cidzudzulo comveka ciposa cikondi cobisika.
6Kulasa kwa bwenzi kulikokhulupirika;
Koma mdani apsompsona kawiri kawiri.
7Mtima wokhuta upondereza cisa ca uci;
Koma wakumva njala ayesa zowawa zonse zotsekemera.
8Monga mbalame yosocera ku cisa cace,
Momwemo munthu wosocera ku malo ace.
9Mafuta ndi zonunkhira zikondweretsa mtima,
Ndi ubwino wa bwenzi uteronso pakupangira uphungu,
10Mnzako, ndi mnzace wa atate wako, usawasiye;
Usanke ku nyumba ya mbale wako tsiku la tsoka lako;
Mnansi wapafupi aposa mbale wakutari.
11Mwananga, khala wanzeru, nukondweretse mtima wanga;
Kuti ndimuyankhe yemwe anditonza.
12Wocenjera aona zoipa, nabisala;
Koma acibwana angopitirira, nalipitsidwa.
13Tenga maraya a woperekera mlendo cikole;
Woperekera mkazi waciwerewere cikole umgwire mwini.
14Yemwe adalitsa mnzace ndi mau akuru pouka mamawa,
Anthu adzaciyesa cimeneco temberero.
15Kudonthadontha tsiku lamvula,
Ndi mkazi wolongolola ali amodzimodzi.
16Wofuna kumletsayo afuna kuletsa mphepo;
Dzanja lace lamanja lingogwira mafuta.
17Citsulo cinola citsulo;
Comweco munthu anola nkhope ya mnzace.
18Wosunga mkuyu adzadya zipatso zace;
Wosamalira ambuyace adzalemekezedwa.
19Monga m'madzi nkhope zionana,
Momwemo mitima ya anthu idziwana.
20Kunsi kwa manda ndi kucionongeko sikukhuta;
Ngakhale maso a munthu sakhutai.
21Siliva asungunuka m'mbiya,
Ndi golidi m'ng'anjo,
Motero comwe munthu acitama adziwika naco.

22Ungakhaleukonolacitsirum'mtondo ndi munsi, pamodzi ndi mphale,
Koma utsiru wace sudzamcoka.
23Udziwitsitse zoweta zako ziri bwanji,
Samalira magulu ako;
24Pakuti cuma siciri cosatha;
Kodi korona alipobe mpaka mibadwo mibadwo?
25Amatuta maudzu, msipu uoneka,
Achera masamba a kumapiri,
26Ana a nkhosa akubveka,
Atonde aombolera munda;
27Mkaka wa mbuzi udzakukwanira kudya;
Ndi a pa banja lako ndi adzakazi ako.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Mau olinganiza zosiyana

1Woipaathawapalibewomthamangitsa;
Koma olungama alimba mtima ngati mkango.
2Pocimwa dziko akalonga ace acuruka;
Koma anthu ozindikira ndi odziwa alikhazikikitsa nthawi yaikuru.
3Munthu waumphawi wotsendereza osauka
Akunga mvula yamadzi yokokolola dzinthu.
4Omwe asiya cilamulo atama oipa;
Koma omwe asunga cilamulo akangana nao.
5Oipa samvetsetsa ciweruzo;
Koma omwe afuna Yehova amvetsetsa zonse.
6Waumphawi woyenda mwangwiro
Apambana ndi yemwe akhotetsa njira zace, angakhale alemera.
7Wosunga cilamulo ndiye mwana wozindikira;
Koma mnzao wa adyera acititsa atate wace manyazi.
8Wocurukitsa cuma cace, pokongoletsa ndi phindu,
Angokundikira yemwe acitira osauka cisoni.
9Wopewetsa khutu lace kuti asamve cilamulo,
Ngakhale pemphero lace linyansa.
10Wosoceretsa oongoka mtima alowe m'njira yoipa,
Adzagwa mwini m'dzenje lace;
Koma angwiro adzalandira colowa cabwino.
11Wolemera adziyesa wanzeru;
Koma wosauka wozindikira aululitsa zace.
12Posekera olungama pali ulemerero wambiri;
Koma pouka oipa anthu amabisala.
13Wobisa macimo ace sadzaona mwai;
Koma wakuwabvomereza, nawasiya adzacitidwa cifundo.
14Wodala munthu wakuopakosalekeza;
Koma woumitsa mtima wace adzagwa m'zoipa.
15Monga mkango wobangula ndi cirombo coyendayenda,
Momwemo mfumu yoipa ya anthu osauka.
16Kalonga wosowa nzeru apambana kusautsa;
Koma yemwe ada cisiriro adzatanimphitsa moyo wace.
17Woparamula mlandu wakupha munthu adzathawira kudzenje;
Asamuletse.
18Woyenda mwangwiro adzapulumuka;
Koma wokhota m'mayendedwe ace adzagwa posacedwa.
19Wolima munda wace zakudya zidzamkwanira;
Koma wotsata anthu opanda pace umphawi udzamkwanira.
20Munthu wokhulupirika ali ndi madalitso ambiri;
Koma wokangaza kulemera sadzapulumuka cilango,
21Cetera siliri labwino,

Ngakhale kulakwa kuti ukadye kanthu.
22Mwini diso lankhwenzule akangaza kulemera,
Osadziwa kuti umphawi udzamfikira.
23Adzamkomera mtima wodzudzula m'tsogolo mwace,
Koposa wosyasyalika ndi lilime lace.
24Wobera atate wace, pena amace, nati, Palibe kulakwa;
Ndiye mnzace wa munthu wopasula.
25Wodukidwa mtima aputa makangano;
Koma wokhulupirira Yehova adzakula.
26Wokhulupirira mtima wace wace ali wopusa;
Koma woyenda mwanzeru adzapulumuka,
27Wogawira aumphawi sadzasowa;
Koma wophimba maso ace adzatembereredwa kwambiri.
28Pouka oipa anthu amabisala;
Koma pakufa amenewo olungama acuruka.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Miyambi 29
1Yemwe aumitsa khosi atadzudzulidwa kwambiri,
Adzasweka modzidzimuka, palibe comciritsa.
2Pocuruka olungama anthu akondwa;
Koma polamulira woipa anthu ausa moyo.
3Mwamuna wokonda nzeru akondweretsa atate wace;
Koma wotsagana ndi akazi adama amwaza cuma.
4Mfumu akhazikitsa dziko ndi ciweruzo;
Koma wosonkhetsa anthu mphatso alipulululutsa.
5Wosyasyalika mnzace Acherera mapazi ace ukonde.
6M'kulakwa kwa woipa muli msampha;
Koma wolungama ayimba, nakondwera.
7Wolungama asamalira mlandu wa osauka;
Koma woipa alibe nzeru yakuudziwa.
8Anthu onyoza atentha mudzi;
Koma anzeru alezetsa mkwiyo.
9Munthu wanzeru akatsutsana ndi munthu wopusa,
Ngakhale akwiya, ngakhale aseka, palibe mtendere.
10Anthu ankhanza ada wangwiro;
Koma oongoka mtima asamalira moyowace.
11Citsiru cibvumbulutsa mkwiyo wace wonse;
Koma wanzeru auletsa nautontholetsa.
12Mkuru akamvera cinyengo,
Atumuki ace onse ali oipa,
13Waumphawi ndi wotsendereza akumana;
Yehova apenyetsa maso a onse awiriwo.
14Mfumu yolamulira osauka mwantheradi,
Mpando wace udzakhazikika kufikira nthawi zonse.
15Ntyole ndi cidzudzulo zipatsa nzeru;
Koma mwana womlekerera acititsa amace manyazi.
16Pocuruka oipa zolakwa zicuruka;
Koma olungama adzaona kugwa kwao.
17Langiza mwana wako, ndipo adzakupumitsa;
Nadzasangalatsa moyo wako.
18Popanda cibvumbulutso anthu amasauka;
Koma wosunga cilamulo adalitsika.
19Kapolo sangalangizidwe ndi mau,
Pakuti azindikira koma osabvomera.
20Kodi uona munthu wansontho m'mau ace?
Ngakhale citsiru cidzacenjera, koma ameneyo ai.
21Yemwe alera kapolo wace mwa ufulu kuyambira ubwana wace,
Pambuyo pace adzadziyesa mwana wobala.
22Mwamuna wamkwiyo aputa makangano;
Waukali acuruka zolakwa.

23Kudzikuza kwa munthu kudzamcepetsa;
Koma wokhala ndi mtima wodzicepetsa adzalemekezedwa.
24Woyenda ndi mbala ada moyo wace wace;
Amva kulumbira, koma osaulula kanthu.
25Kuopa anthu kuchera msampha;
Koma wokhulupirira Yehova adzapulumuka,
26Ambiri afunafuna ciyanjano ca mkuru;
Koma ciweruzo ca munthu cicokera kwa Yehova.
27Munthu woipa anyansa olungama;
Ndipo woongoka m'njira anyansa wocimwa.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Cibvomerezo, pemphero ndi malangizo a Aguri

1Mau a Aguri mwana wa Yake; uthenga. Munthuyo anati,
Ndadzitopetsa, Mulungu;
Ndadzitopetsa, Mulungu, ndathedwa;
2Pakuti ndipambana anthu onse kupulukira,
Ndiribe luntha la munthu.
3Sindinaphunzira nzeru
Ngakhale kudziwa Woyerayo.
4Ndani anakwera kumwamba natsikanso?
Ndani wakundika nafumbata mphepo?
Ndani wamanga madzi m'maraya ace?
Ndani wakhazikitsa matsiriziro onse a dziko?
Dzina lace ndani? dzina la mwanace ndani? kapena udziwa.
5Mau onse a Mulungu ali oyengeka;
Ndiye cikopa ca iwo amene amkhulupirira.
6Usaoniezere kanthu pa mau ace,
Angakudzudzule, nungatsutsidwe kuti ulikunama.
7Zinthu ziwiri ndakupemphani,
Musandimane izo ndisanamwalire:
8Mundicotsere kutari zacabe ndi mabodza;
Musandipatse umphawi, ngakhale cuma,
Mundidyetse zakudya zondiyenera;
9Ndingakhute ndi kukukanani, ndi kuti, Yehova ndani?
Kapena ndingasauke ndi kuba,
Ndi kuchula dzina la Mulungu wanga pacabe.
10Usanamizire kapolo kwa mbuyace,
Kuti angakutemberere nawe ndi kutsutsidwa.
11Pali mbadwo wotemberera atate ao,
Osadalitsa amao.
12Pali mbadwo wodziyesa oyera,
Koma osasamba litsilo lao.
13Pali mbadwo wokwezatu maso ao,
Zikope zao ndi kutukula.
14Pali mbadwo mano ao akunga malupanga, zibwano zao zikunga mipeni;
Kuti adye osauka kuwacotsa kudziko, ndi aumphawi kuwacotsa mwa anthu.
15Msundu uli ndi ana akazi awiri ati, Patsa, patsa,
Pali zinthu zitatu sizikhuta konse,
Ngakhale zinai sizinena, Kwatha:
16Manda, ndi cumba,
Dziko losakhuta madzi,
Ndi moto wosanena, Kwatha.

17Diso locitira atate wace ciphwete, ndi kunyoza kumvera amace,
Makungubwi a kumtsinje adzalikolowola, ana a mphungu adzalidya,
18Zinthu zitatu zindithetsa nzeru,
Ngakhale zinai, sindizidziwa:
19Njira ya mphungu m'mlengalenga,
Njira ya njoka pamwala,
Njira ya ngalawa pakati pa nyanja.
Njira ya mwamuna ndi namwali.
20Comweco njira ya mkazi wacigololo;
Adya, napukuta pakamwa, nati, Sindinacita zoipa,
21Cifukwa ca zinthu zitatu dziko linthunthumira;
Ngakhale cifukwa ca zinai silingathe kupirira nazo:
22Cifukwa ca kapolo pamene ali mfumu;
Ndi citsiru citakhuta zakudya;
23Cifukwa ca mkazi wodedwa wokwatidwa;
Ndi mdzakazi amene adzalandira colowa ca mbuyace.
24Ziripo zinai ziri zazing'ono padziko;
Koma zipambana kukhala zanzeru:
25Nyerere ndi mtundu wosalimba,
Koma zitengeratu zakudya zao m'malimwe.
26Mbira ndi mtundu wopanda mphamvu,
Koma ziika nyumba zao m'matanthwe.
27Dzombe liribe mfumu,
Koma lituruka lonse mabwalo mabwalo.
28Buluzi ungamgwire m'manja,
Koma ali m'nyumba za mafumu.
29Pali zinthu zitatu ziyenda cinya cinya;
Ngakhale zinai ziyenda mwaufulu:
30Mkango umene uposa zirombo kulimba,
Supambukira cinthu ciri conse;
31Kavalo wolimba m'cuuno, ndi tonde,
Ndi mfumu yokhala ndi ankhondo ace.
32Ngati wapusa podzikweza,
Ngakhale kuganizira zoipa, tagwira pakamwa.
33Pakuti potakasa mkaka, mafuta ayengekapo;
Ndi popsinja mpfuno, mwazi uturukamo;
Ndi potimbikira mkwiyo ndeu ionekamo.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Malangizo a mai wa Lemueli

1Mau a Lemueli mfumu, uthenga umene amace anamphunzitsa.
2Ciani mwananga, Ciani mwana wa mimba yanga?
Ciani mwana wa zowinda zanga?
3Musapereke mphamvu yako kwa akazi,
Ngakhale kuyenda m'njira yoononga mafumu.
4Mafumu, Lemueli, mafumu sayenera kumwa vinyo;
Akalonga sayenera kunena, Cakumwa caukali ciri kuti?
5Kuti angamwe, naiwale malamulo,
Naweruze mokhota anthu onse osautsidwa.
6Wofuna kufa umpatse cakumwa caukali,
Ndi vinyo kwa owawa mtima;
7Amwe, narwale umphawi wace, Osakumbukiranso bvuto lace.
8Tsegula pakamwa pako, ukanenere wosalankhula,
Ndi mlandu wa amasiye onse.
9Tsegula pakamwa pako,
Nuweruze molungama, nunenere osauka ndi aumphawi.
10Mkazi wangwiro ndani angampeze?
Pakuti mtengo wace uposa ngale.
11Mtima wa mwamuna wace umkhulupirira,
Sadzasowa phindu.
12Mkaziyo amcitira zabwino, si zoipa,
Masiku onse a moyo wace.
13Afuna ubweya ndi thonje,
Nacita mofunitsa ndi manja ace.
14Akunga zombo za malonda;
Nakatenga zakudya zace kutari.
15Aukanso kusanace,
Napatsa banja lace zakudya, nagawira adzakazi ace nchito.
16Asinkhasinkha za munda, naugula;
Naoka mipesa ndi zipatso za manja ace.
17Amanga m'cuuno mwace ndi mphamvu,
Nalimbitsa mikono yace,
18Azindikira kuti malonda ace ampindulira;
Nyali yace sizima usiku.
19Agwira njinga ya thonje ndi dzanja lace,
Nafumbata mtengo wace.
20Aolowera cikhato cace osauka;
Natambasulira aumphawi manja ace.
21Saopera banja lace cipale cofewa;
Pakuti banja lace lonse libvala mlangali.
22Adzipangira zimbwi zamaangamaanga;
Nabvala bafuta ndi guta woti biriwiri.

23Mwamuna wace adziwika kubwalo,
Pokhala pakati pa akuru a dziko.
24Asoka maraya abafuta, nawagulitsa;
Napereka mipango kwa wogulitsa malonda.
25Abvala mphamvu ndi ulemu;
Nangoseka nthawi ya m'tsogolo.
26Atsegula pakamwa pace ndi nzeru,
Ndipo cilangizo ca cifundo ciri pa lilime lace.
27Ayang'anira mayendedwe a banja lace,
Sadya zakudya za ulesi.
28Anace adzanyamuka, nadzamucha wodala;
Mwamuna wace namtama, nati,
29Ana akazi ambiri anacita mwangwiro,
Koma iwe uposa onsewo.
30Kukongola kungonyenga, maonekedwe okoma ndi cabe;
Koma mkazi woopa Yehova adzatamandidwa.
31Mumpatse zipatso za manja ace; Ndi nchito zace zimtame
kubwalo.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Ecclesiastes

Mlaliki 1

Za pansi pano nzacabe

1MAU a Mlaliki, mwana wa Davide, mfumu ya
m'Yerusalemu. 2Zacabecabe, ati Mlaliki; zacabecabe zonse ndi
cabe. 3Kodi nchito zace zonse munthu asauka nazo zimpindulira
ciani? 4Mbadwo wina opita, mbadwo wina nufika; koma dziko
lingokhalabe masiku onse, 5inde dzuwa lituruka, nililowa,
nilifulumira komwe linaturukako. 6Kulowa kumwela ndi kuzungulira:
kumpoto zungulire zungulire imaomba mphepo; ibweranso monga
mwa mazunguliridwe ace. 7Mitsinje yonse ithira m'nyanja, koma
nyanja yosadzala; komwe imukira mitsinjeyo, komweko
ibweranso. 8Zinthu zonse zilemetsa; munthu sakhoza kuzifotokoza;
maso sakhuta m'kuona, ndi makutu sakhuta m'kumva. 9Comwe
cinaoneka cidzaonekanso; ndi comwe cinacitidwa cidzacitidwanso;
ndipo palibe kanthu katsopano pansi pano. 10Kodi pali kanthu
unganene kuti, Taona katsopano aka? Kanalipo kale, kale lomwe
tisanabadwe ife. 11Zoyamba zija sizikumbukiridwa; ngakhale
zomwe zirinkudzazo, omwe adzakhalabe m'tsogolomo,
sadzazikumbukirai.
12Ine Mlaliki ndinali mfumu ya: Israyeli m'Yerusalemu. 13Ndipo
ndinapereka mtima kufunafuna ndi nzeru, ndi kulondetsa zonse
zimacitidwa pansi pa thambo; nchito yobvuta imeneyi Mulungu
apatsa ana a anthu akasauke nayo. 14Ndaona nchito zonse
zipangidwa kunja kuno; ndipo zonsezo ndi cabe ndi kungosautsa
mtima. 15Cokhotakhota sicingaongokenso; ndipo coperewera
sicingawerengedwe. 16Ndinalankhula ndi mtima wanga, ndi kuti,
Taona, ndakuza ndi kudzienjezera nzeru koposa onse anakhala
m'Yerusalemu ndisanabadwe ine; inde mtima wanga wapenyera
kwambiri nzeru ndi cidziwitso. 17Ndipo ndinapereka mtima kudziwa
nzeru ndi kudziwa misala ndi utsiru; ndinazindikira kuti icinso
cingosautsa mtima. 18Pakuti m'nzeru yambiri muli cisoni cambiri;
ndi yemwe aenjezera cidziwitso aenjezera zowawa.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Mliliki 2

Za m'moyo uno sizitha kukondweretsa mtima

1Ndinati mumtima mwanga, Tiyetu, ndikuyese ndi cimwemwe; tapenya tsono
zabwino; ndipo taona, icinso ndi cabe. 2Ndinati, Kuseka ndi misala; ndi
cimwemwe kodi cicita ciani? 3Ndinafuna mumtima mwanga kusangalatsa
thupi langa ndi vinyo, mtima wanga ulikunditsogolera mwanzeru, ndi kugwira
utsiru, kuti ndizindikire cabwinoco ca ana a anthu nciani cimene azicicita
pansi pa thambo masiku onse a moyo wao. 4Ndinadzipangira zazikuru;
ndinadzimangira nyumba; ndi kunka mipesa; 5ndinakonza mphanie ndi minda
yanga, ndi kuokamo mitengo ya zipatso za mitundu
mitundu; 6ndinadzipangira ndekha matamanda a madzi akuthirira madzi
m'nkhalango momeramo mitengo; 7ndinadzitengera akapolo ndi adzakazi,
ndinali ndi akapolo anabadwa kwanga; ndinalemeranso pokhala nazo zoweta
zazikuru ndi zazing'ono kupambana onse anakhala m'Yerusalemu
ndisanabadwe ine; 8ndinakundikanso siliva ndi golidi ndi cuma ca mafumu ndi
madera a dziko; ndinaitanitsa amuna ndi akazi akuyimba ndi zokondweretsazo
za ana a anthu, ndizo zoyimbira za mitundu mitundu. 9Ndinakula cikulire
kupambana onse anali m'Yerusalemu ndisanabadwe ine; ndipo nzeru
yanganso inakhala nanebe. 10Ndipo ciri conse maso anga anacifuna
sindinawamana; sindinakaniza mtima wanga cimwemwe ciri conse pakuti
mtima wanga unakondwera ndi nchito zanga zonse; gawo langa la m'nchito
zanga zonse ndi limeneli. 11Pamenepo ndinayang'ana zonse manja anga
anazipanga, ndi nchito zonse ndinasauka pozigwira; ndipo taona, zonse zinali
zacabecabe ndi kungosautsa mtima, ndipo kunalibe phindu kunja kuno.
12Ndipo ndinatembenuka kukayang'ana nzeru ndi misala ndi utsiru; pakuti
yemwe angotsata mfumu angacite ciani? Si comwe cinacitidwa
kale. 13Pamenepo ndinazindikira kuti nzeru ipambana utsiru kwambiri, monga
kuunika kupambana mdima. 14Wanzeru maso ace ali m'mutu wace, koma
citsiru ciyenda mumdima; ndipo nanenso ndinazindikira kuti comwe
ciwagwera onsewo ndi cimodzi. 15Pamenepo ndinati mumtima mwanga,
Comwe cigwera citsiru nanenso cindigwera; nanga bwanji ndinapambana
kukhala wanzeru? Pamenepo ndinati mumtima mwanga kuti icinso ndi
cabe. 16Pakuti wanzerusaposa citsiru kukumbukidwa nthawi zonse; pakuti
zonse zooneka kale zidzaiwalika m'tsogolomo, Ndipo wanzeru amwalira bwanji
ngati citsirutu. 17Cifukwa cace ndinada moyo; pakuti nchito azipanga kunja
kuno zindisautsa; pakuti zonse ndi cabe ndi kungosautsa mtima.
18Ndipo ndinada nchito zanga zonse ndinasauka nazo kunja kuno; pakuti
ndidzamsiyira izo munthu wina amene adzanditsata. 19Ndipo ndani adziwa
ngati adzakhala wanzeru pena citsiru? Koma adzalamulira nchito zanga zonse
ndinasauka nazo, ndi kuzigwira mwanzeru kunja kuno. Icinso ndi
cabe. 20Ndipo ndinatembenuka ndi kukhululuka za nchito zanga zonse
ndasauka nazo kunja kuno. 21Pakuti pali munthu wina agwira nchito
mwanzeru ndi modziwa nadzipinduliramo; koma adzapereka gawo lace kwa
munthu amene sanagwirapo nchito. Icinso ndi cabe ndi coipa
cacikuru. 22Pakuti munthu ali ndi ciani m'nchito zace zonse, ndi m'kusauka
kwa mtima wace amasauka nazozo kunja kuno? 23Pakuti masiku ace onse ndi
zisoni, bvuto lace ndi kumliritsa; ngakhale usiku mtima wace supuma. Icinso
ndi cabe.
24Kodi si cabwino kuti munthu adye namwe, naonetse moyo wace, zabwino
m'nchito yace? icinso ndinacizindikira kuti cicokera ku dzanja la
Mulungu. 25Pakuti ndani angadye ndi kufulumirako, koposa ine. 26Pakuti
yemwe Mulungu amuyesa wabwino ampatsa nzeru ndi cidziwitso ndi

cimwemwe; koma wocimwa amlawitsa bvuto la kusonkhanitsa ndi kukundika, kuti aperekere yemwe Mulungu amuyesa wabwino. Icinso ndi cabe ndi kungosautsa mtima.

Ziri zofise ziri ndi nyengo yace, Mulungu ndi kuziika zonse

1Kanthu kali konse kali ndi nthawi yace ndi cofuna ciri conse ca
pansi pa thambo ciri ndi mphindi yace; 2mphindi yakubadwa ndi
mphindi yakumwalira; mphindi yakubzyala ndi mphindi yakuzula
zobzyalazo; 3mphindi yakupha ndi mphindi yakuciza; mphindi
yakupasula ndi mphindi yakumanga; 4mphindi yakugwa misozi ndi
mphindi yakuseka; mphindi yakulira ndi mphindi
yakubvina; 5mphindi yakutaya miyala ndi mphindi yakukundika
miyala; mphindi yakufungatirana ndi mphindi yakuleka
kufungatirana; 6mphindi yakufunafuna ndi mphindi yakumwazika;
mphindi yakusunga ndi mphindi yakutaya; 7mphindi yakung'amba
ndi mphindi yakusoka; mphindi yakutonthola ndi mphindi
yakulankhula; 8mphindi yakukonda ndi mphindi yakudana; mphindi
ya nkhondo ndi mphindi ya mtendere. 9Wogwira nchito aona
phindu lanji m'comsautsaco? 10Ndaona bvuto limene Mulungu
wapatsa ana a anthu kuti abvutidwe nalo. 11Cinthu ciri conse
anacikongoletsa pa mphindi yace; ndipo waika zamuyaya
m'mitima yao ndipo palibe munthu angalondetse nchito Mulungu
wazipanga ciyambire mpaka citsiriziro. 12Ndidziwa kuti iwo alibe
ubwino, koma kukondwa ndi kucita zabwino pokhala ndi
moyo. 13Ndiponso kuti munthu yense adye namwe naone zabwino
m'nchito zace zonse; ndiwo mtulo wa Mulungu. 14Ndidziwa kuti
zonse Mulungu azicita zidzakhala kufikira nthawi zonse;
sungaonjezepo kanthu, ngakhale kucotsapo; Mulungu nazicita kuti
anthu akaope pamaso pace. 15Cocomwe cinaoneka, cirikuonekabe;
ndi comwe cidzaoneka cinacitidwa kale; Mulungu anasanthula
zocitidwa kale.
16Ndiponso ndinaona kunja kuno malo akuweruza, komweko kuli
zaipa; ndi malo a cilungamo, komweko kuli zoipa. 17Ndinati
mumtima wanga, Mulungu adzaweruza wolungama ndi woipa;
pakuti pamenepo pali mphindi ya zofuna zonse ndi nchito
zonse. 18Ndinati mumtima mwanga, kuti izi zicitika ndi ana a
anthu, kuti Mulungu awayese ndi kuti akazindikire eni ace kuti
ndiwo nyama za kuthengo. 19Pakuti comwe cigwera ana a anthu
cigweranso nyamazo; ngakhale cowagwera ncimodzimodzi; monga
winayo angofa momwemo zinazo zifanso; inde onsewo ali ndi
mpweya umodzi; ndipo munthu sapambana nyama pakuti zonse
ndi cabe, 20onse apita ku malo amodzi; onse acokera m'pfumbi ndi
onse abweranso kupfumbi. 21Ndani adziwa mzimu wa ana a anthu
wakwera kumwamba, ndi mzimu wa nyama wotsikira kunsi ku
dziko? 22M'mwemo ndinazindikira kuti kulibe kanthu kabwino
kopambana aka, kuti munthu akondwere ndi nchito zace; pakuti

gawo lace ndi limeneli; pakuti ndani adzamfikitsa kuona comwe cidzacitidwa ataca iyeyo?

©The Bible Society of Malawi, 1992

Matsoka ndi mabvuto a moyo uno

1Ndinabweranso tsono ndi kupenyera nsautso zonse zimacitidwa
kunja kuno; ndipo taona, misozi ya otsenderezedwa, koma analibe
wakuwatonthoza; ndipo akuwatsendereza anali ndi mphamvu
koma iwowa analibe wakuwatonthoza. 2Ndipo ndinatama akufa
atatha kufa kupambana amoyo omwe alipobe; 3inde yemwe
sanabadwe konse aposa onse awiriwo popeza sanaone nchito
yoipa yocitidwa kunja kuno.
4Ndiponso ndinapenyera mabvuto onse ndi nchito zonse
zompindulira bwino, kuti cifukwa ca zimenezi anansi ace acitira
munthu nsanje. Icinso ndi cabe ndi kungosautsa mtima. 5Citsiru
cimanga manja ace, nicidya nyama yace yace. 6Dzanja limodzi
lodzala pali mtendere liposa manja awiri oti tho pali bvuto ndi
kungosautsa mtima.
7Pamenepo ndinabwera ndi kupenyera zacabe kunja kuno. 8Pali
mmodzi palibe waciwiri; inde, alibe mwana ngakhale mbale; koma
nchito yace yonse iribe citsiriziro, ngakhale diso lace silikhuta
cuma. Samati, Ndigwira nchito ndi kumana moyo wanga zabwino
cifukwa ca yani? Icinso ndi cabe, inde, bvuto lalikuru. 9Awiri aposa
mmodzi; pakuti ali ndi mphotho yabwino m'nchito zao. 10Pakuti
akagwa, wina adzautsa mnzace; koma tsoka wakugwa wopanda
womnyamutsa. 11Ndiponso awiri akagona limodzi afunditsana;
koma mmodzi pa yekha kodi adzafunditsidwa bwanji? 12Ndipo wina
akamlaka mmodziyo, awiri adzacirimika; ndipo cingwe ca nkhosi
zitatu siciduka msanga.
13Mnyamata wosauka ndi wanzeru apambana mfumu yokalamba
ndi yopusa, imene sifunanso kulangidwa mwambo. 14Pakuti
aturuka m'nyumba yandende kulowa ufumu; komanso yemwe
abadwa m'dziko lace asauka. 15Ndinapenyera anthu onse amoyo
akuyenda kunja kuno, kuti anali ndi mwana, waciwiri, amene
adzalowa m'malo mwace. 16Anthu onse sawerengeka, ngakhale
onsewo anawalamulira; koma amene akudza m'mbuyo
sadzakondwera naye. Icinso ndi cabe nicisautsa mtima.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Malangizo osiyana akuwasamalira anthu m'moyo uno

1Samalira phazi lako popita ku nyumba ya Mulungu; pakuti
kuyandikira kumvera kupambana kupereka nsembe za zitsiru;
pakuti sizizindikira kuti zirikucimwa. 2Usalankhule mwanthuku
mtima wako, usafulumire kunena kanthu pamaso pa Mulungu;
pakuti Mulungu ali kumwamba, iwe uli pansi; cifukwa cace mau
ako akhale owerengeka. 3Pakuti loto lafika mwakucuruka nchito;
ndipo mau a citsiru mwakucuruka maneno. 4Utawinda ciwindo kwa
Mulungu, usacedwe kucicita; pakuti sakondwera ndi zitsiru; cita
comwe unaciwindaco. 5Kusawinda kupambana kuwinda
osacita, 6Usalole m'kamwa mwako mucimwitse thupi lako;
usanene pamaso pa mthenga kuti, Ndinaphophonya; Mulungu
akwiyire mau ako cifukwa ninji, naononge nchito ya manja
ako? 7Pakuti monga mu unyinji wa maloto muli zacabe motero
mocuruka mau; koma dziopa Mulungu.
8Ukaona anthu alikutsendereza aumphawi, ndi kucotsa cilungamo
ndi ciweruzo mwaciwawa pa dera lina la dziko, usazizwepo; pakuti
mkuru wopambana asamalira; ndipo alipo akuru ena oposa
amenewo. 9Phindutu la dziko lipindulira onse; ngakhale mfumu
munda umthandiza.
10Wokonda siliva sadzakhuta siliva; ngakhale wokonda cuma
sadzakhuta phindu; icinso ndi cabe. 11Pocuruka katundu, akudyapo
acurukanso; nanga apindulira eni ace ciani, koma kungopenyera
ndi maso ao? 12Tulo ta munthu wogwira nchito ntabwino, ngakhale
adya pang'ono ngakhale zambiri; koma kukhuta kwa wolemera
sikumgonetsa tulo.
13Pali coipa cobvuta ndaciona kunja kuno, ndico, cuma
cirikupweteka eni ace pocikundika; 14koma cumaco cionongeka
pomgwera tsoka; ndipo akabala mwana, m'dzanja lace mulibe
kanthu. 15Monga anaturuka m'mimba ya amace, adzabweranso
kupita wamarisece, monga anadza osatenga kanthu pa nchito
zace, kakunyamula m'dzanja lace. 16Icinso ndi coipa cowawa,
cakuti adzangopita monse monga anadza; ndipo wodzisautsa cabe
adzaona phindu lanji? 17Inde masiku ace onse amadya mumdima,
nizimcurukira cisoni ndi nthenda ndi mkwiyo.
18Taonani, comwe ine ndapenyera kukoma ndi kuyenera munthu
ndiko kudya, ndi kumwa, ndi kukondwera ndi nchito zace zonse
asauka nazo kunja kuno, masiku onse a moyo wace umene
Mulungu ampatsa; pokhala gawo lace limeneli. 19Inde yemwe
Mulungu wamlemeretsa nampatsa cuma, namninkhanso mphamvu
ya kudyapo, ndi kulandira gawo lace ndi kukondwera ndi nchito
zace; umenewu ndiwo mtulo wa Mulungu. 20Pakuti

sadzakumbukira masiku a moyo wace kwambiri; cifukwa Mulungu ambvomereza m'cimwemwe ca mtima wace.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Ngakhale Mulungu apatsa munthu zonse azikhumba koma mtima sukhuta nazo

1Pali coipa ndaciona kunja kuno cifalikira mwa anthu, 2munthu
amene Mulungu wamlemeretsa nampatsa cuma ndi ulemu, mtima
wace susowa kanthu kena ka zonse azifuna, koma Mulungu
osampatsa mphamvu ya kudyapo, koma mlendo adyazo; ici ndi
cabe ndi nthenda yoipa, 3Cinkana munthu akabala ana makumi
khumi, nakhala ndi moyo zaka zambiri, masiku a zaka zace ndi
kucuruka, koma mtima wace osakhuta zabwino, ndiponso alibe
maliro; nditi, Nsenye iposa ameneyo; 4pakuti ikudza mwacabe,
nicoka mumdima, mdima nukwirira dzina lace. 5Ngakhale dzuwa
siliona ngakhale kulidziwa, imeneyi ipambana winayo
kupuma; 6akakhala ndi moyo zaka zikwi ziwiri, koma osakondwera;
kodi onse sapita ku malo amodzi? 7Nchito zace zonse munthu
angogwirira m'kamwa mwace, koma mtima wace sukhuta. 8Pakuti
wanzeru ali ndi ciani coposa citsiru? Waumphawi wodziwa kuyenda
pa maso pa amoyo ali ndi ciani? 9Kupenya kwa maso kuposa
kukhumba kwa mtima; icinso ndi cabe ndi kungosautsa mtima.
10Comwe cinalipo cachedwa dzina lace kale, cidziwika kuti ndiye
munthu; sakhoza kulimbana ndi womposa mphamvu. 11Pokhala
zinthu zambiri zingocurukitsa zacabe, kodi anthu aona phindu
lanji? 12Pakuti ndani adziwa comwe ciri cabwino kwa munthu ali
ndi moyo masiku onse a moyo wace wacabe umene autsiriza ngati
mthunzi? pakuti ndani adzauza munthu cimene cidzaoneka
m'tsogolo mwace kunja kuno?

©The Bible Society of Malawi, 1992

Kumva zowawa nkokoma, nzeru ndi kudziletsa momwemo

1Mbiri yabwino iposa zonunkhira zabwino; ndi tsiku lakumwalira
liposa tsiku lakubadwa. 2Kunka ku nyumba ya maliro kupambana
kunka ku nyumba ya madyerero; pakuti kujako ndi matsiriziro a
anthu onse; ndipo omwe ali ndi moyo adzakumbukirapo. 3Cisoni
ciposa kuseka; pakuti nkhope yakugwa ikonza mtima. 4Mtima wa
anzeru uli m'nyumba ya maliro; koma mtima wa zitsiru uli
m'nyumba ya kuseka. 5Kumva cidzudzulo ca anzeru kupambana
kumva nyimbo ya zitsiru. 6Pakuti kuseka kwa citsiru kunga minga
irikutetheka pansi pa mphika; icinso ndi cabe. 7Indetu nsautso
iyarutsa wanzeru; ndi mtulo uipitsa mtima. 8Citsiriziro ca kanthu
ciposa ciyambi cace; wofatsa mtima apambana wodzikuza
mtima. 9Usakangaze mumtima mwako kukwiya; pakuti mkwiyo
ugona m'cifuwa ca zitsiru. 10Usanene, Kodi bwanji masiku akale
anapambana ano? Pakuti sulikufunsa mwanzeru
pamenepo. 11Nzeru iri yabwino pamodzi ndi colowa; akuona dzuwa
apindula nayo. 12Pakuti nzeru icinjiriza monga ndalama zicinjiriza;
koma kudziwa kupambana, cifukwa nzeru isunga moyo wa eni
ace. 13Tapenya nchito ya Mulungu; pakuti ndani akhoza
kulungamitsa comwe iye anacikhotetsa? 14Tsiku la mwai kondwera,
koma tsiku la tsoka lingirira; Mulungu waika ici pambali pa cinzace,
kuti anthu asapeze kanthu ka m'tsogolo mwao.
15Ndaona zonsezi masiku anga acabe; pali wolungama angofa
m'cilungamo cace, ndipo pali woipa angokhalabe ndi moyo
m'kuipa kwace. 16Usapambanitse kukhala wolungama; usakhale
wanzeru koposa; bwanji ufuna kudziononga
wekha? 17Usapambanitse kuipa, ngakhale kupusa, uferenji nthawi
yako isanafike? 18Kuli kwabwino kugwira ici; indetu, usacotsepo
dzanja lako pakuti yemwe aopa Mulungu adzaturuka monsemo.
19Nzeru ilimbitsa wanzeru koposa akuru khumi akulamulira
m'mudzi. 20Pakuti kulibe wolungama pansi pano amene acita
zabwino osacimwa. 21Mau onsetu onenedwa usawalabadire; kuti
usamve kapolo wako alikukutemberera; 22pakuti kawiri kawiritu
mtima wako udziwa kuti nawenso unatemberera ena.
23Ndayesa zonsezi ndi nzeru; ndinati, Ndidzakhala wanzeru, koma
inanditarikira. 24Cakutari ndi cakuyadi adzacipeza
ndani? 25Ndinapotoka ndi mtima wanga womwe kudziwa ndi
kusanthula ndi kufunafuna nzeru ndi malongosoledwe a zinthu, ndi
kudziwa kuti udio ndiwo utsiru, ndi kuti kupusa ndi misala; 26ndipo
ndinapeza kanthu kowawa koposa imfa, ndiko mkazi amene ndiye
msampha, mtima wace ukunga maukonde, manja ace ndiwo
matangadza; yemwe Mulungu amuyesa wabwino adzapulumuka
kwa iye; koma wocimwa adzagwidwa naye. 27Taonani, ici

ndacipeza, ati Mlalikiyo, m'kuphatikiza cinthu cina ndi cinzace,
ndikazindikire malongosoledwe ao; 28comwe moyo wanga ucifuna
cifunire, koma osacipezai ndi ici, mwamuna mmodzi mwa cikwi
ndinampezadi, koma mkazitu mwa onsewo
sindinampeza. 29Taonani, ici cokha ndacipeza kuti Mulungu
analenga anthu oongoka mtima; koma iwowo afunafuna
malongosoledwe a mitundu mitundu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Langizo la kumvera mfumu

1Ndani akunga wanzeru? Ndani adziwa tanthauzo la mau? Nzeru
ya munthu iwalitsa nkhope yace, kuduwa kwa nkhope yace ndi
kusanduka. 2Nditi, Sunga mau a mfumu, makamaka m'kulumbira
Mulungu. 3Usakangaze kumcokera; usaumirire kanthu koipa; pakuti
iyeyo amacita comwe cimkonda. 4Pakuti mau a mfumu ali ndi
mphamvu; ndipo ndani anganene kwa iye, Kodi ucita
ciani? 5Wosunga cilamulo sadzadziwa kanthu koipa; ndipo mtima
wa munthu wanzeru udziwa nyengo ndi maweruzo; 6pakuti kanthu
kali konse kali ndi nthawi yace ndi ciweruzo cace; popeza zoipa za
munthu zimcurukira; 7pakuti sadziwa cimene cidzakhala; pakuti
ndani angamuuze nthawi yakuti cidzacitidwa? 8Kulibe munthu ali
ndi mphamvu yolamulira mzimu ndi yakutsekereza mzimu;
ngakhale mphamvu tsiku la imfa; munkhondo umo mulibe
kumasuka; udio sudzapulumutsa akuzolowerana nao. 9Zonsezi
ndaziona ndi kuyang'anitsa mtima wanga nchito zonse zicitidwa
pansi pano; nthawi yakuti wina apweteka mnzace pomlamulira.

Woipa salangidwa pakucita pomwepo; mwina wolungama aona nsautso

10Ndipo ndinaona oipa alikuikidwa m'manda ndi kupita; ndipo
omwe anacita zolungama anacokera ku malo opatulika a ku mudzi
nawaiwala; icinso ndi cabe. 11Popeza sambwezera coipa cace
posacedwa atamtsutsa munthu, ana a anthu atsimikizadi mitima
yao kucita zoipa. 12Angakhale wocimwa acita zoipa zambirimbiri,
masiku ace ndi kucuruka, koma ndidziwitsadi kuti omwe aopa
Mulungu naopa pamaso pace adzapeza bwino; 13koma woipa
sadzapeza bwino ngakhale kutanimphitsa masiku ace ngati
mthunzi; cifukwa saopa pamaso pa Mulungu. 14Pali cinthu cacabe
cimacitidwa pansi pano; cakuti alipo olungama amene aona
zomwe ziyenera nchito za oipa, ndipo alipo oipa amene aona
zomwe ziyenera nchito za olungama, Ndinati, Icinso ndi
cabe. 15Pompo ndinatama kusekaseka, pakuti munthu alibe kanthu
kabwino pansi pano, koma kudya ndi kumwa, ndi kusekera; ndi kuti
zimenezi zikhalebe naye m'bvuto lace masiku onse a moyo wace
umene Mulungu wampatsa pansi pano. 16Pompo ndinapereka
mtima wanga kudziwa nzeru, ndi kupenya nchito zicitidwa pansi
pano; kuti anthu saona tulo konse ndi maso ao ngakhale usana
ngakhale usiku; 17pamenepo ndinaona nchito zonse za Mulungu
kuti anthu sangalondole nchito zicidwa pansi pano; pakuti
angakhale munthu ayesetsa kuzifunafuna koma sadzazipeza;
indetu ngakhalenso wanzeru akati, ndidziwa, koma adzalephera
kuzilondola.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Okoma ndi oipa amamva zomwezo. Khalani nazo zakupatsa Mulungu mokondwera

1Pakuti zonsezi ndinazisunga mumtima ndikalondoletu zonsezi;
kuti olungama ndi anzeru ndi nchito zao ali m'manja a Mulungu;
ngakhale kukonda ngakhale kudana anthu sadziwa; zonse ziri
m'tsogolo mwao. 2Zonse zigwera onse cimodzimodzi; kanthu
kamodzi kangogwera wolungama ndi woipa; ngakhale wabwino ndi
woyera ndi wodetsedwa: ngakhale wopereka nsembe ndi
wosapereka konse; wabwino alingana ndi wocimwa; wolumbira ndi
woopa lumbiro. 3Ici ndi coipa m'zonse zicitidwa pansi pano, cakuti
kanthu kamodzi kagwera onse; indetu, mtimanso wa ana a anthu
wadzala udio, ndipo misala iri m'mtima wao akali ndi moyo, ndi
pamenepo apita kwa akufa. 4Pakuti woyang'ana ndi amoyo onse ali
naco ciyembekezo; pakuti garu wamoyo aposa mkango
wakufa. 5Pakuti amoyo adziwa kuti tidzafa; koma akufa sadziwa
kanthu bi, sadzalandira mphotho; pakuti angoiwalika. 6Cikondi cao
ndi mdano wao ndi dumbo lao lomwe zatha tsopano; ndipo nthawi
yamuyaya sagawa konse kanthu kali konse kacitidwa pansi pano.
7Tiye, idya zakudya zako mokondwa, numwe vinyo wako mosekera
mtima; pakuti Mulungu wabvomerezeratu zocita zako. 8Zobvala
zako zikhale zoyera masiku onse; mutu wako usasowe
mafuta. 9Khalani mokondwa ndi mkazi umkonda masiku onse a
moyo wako wacabe, umene Mulungu wakupatsa pansi pano
masiku ako onse acabe; pakuti ilo ndi gawo lako la m'moyo ndi
m'nchito zimene ubvutika nazo pansi pano. 10Ciri conse dzanja
lako licipeza kucicita, ucicite ndi mphamvu yako; pakuti mulibe
nchito ngakhale kulingirira ngakhale kudziwa, ngakhale nzeru,
kumanda ulikupitako.

Nzeru ya mwini ilanditsa ena

11Ndinabweranso ndi kuzindikira pansi pano kuti omwe atamanga
msanga sapambana m'liwiro, ngakhale olimba sapambana
m'nkhondo, ngakhale anzeru sapeza zakudya, ngakhale ozindikira
bwino salemera, ngakhale odziwitsa sawakomera mtima; koma
yense angoona zomgwera m'nthawi mwace. 12Pakuti munthu
sadziwatu mphindi yace; monga nsomba zigwidwa m'ukonde
woipa, ndi mbalame zikodwa mumsampha, momwemo ana a
anthu amagwidwa ndi nthawi ya tsoka, ngati msampha umene
uwagwera modzidzimuka.
13Ndaonanso nzeru pansi pano motero, ndipo inandionekera
yaikuru; 14panali mudzi waung'ono muli anthu owerengeka; ndipo
inadzako mfumu yaikuru, niizinga ndi nkhondo, nimangapo
malinga akuru; 15koma anapezedwamo mwamuna wanzeru
wosauka, yemweyo napulumutsa mudziwo ndi nzeru yace; koma

panalibe anthu anakumbukira wosauka ameneyo. 16Pamenepo
ndinati, Nzeru ipambana mphamvu; koma anyoza nzeru ya
wosauka, osamvera mau ace.
17Mau a anzeru acete amveka koposa kupfuula kwa wolamulira
mwa zitsiru. 18Nzeru ipambana zida za nkhondo; koma wocimwa
mmodzi aononga zabwino zambiri.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Kupusa kusautsa kwambiri

1Nchenche zakufa zinunkhitsa moipa nizioletsa mafuta onunkhira a
sing'anga; comweco kupusa kwapang'ono kuipitsa iye amene
achuka cifukwa ca nzeru ndi ulemu. 2Wanzeru, mtima wace uli ku
dzanja lace lamanja; koma citsiru, mtima wace
kulamanzere. 3Inde, poyendanso citsiru panjira, nzeru yace
imthera ndipo angoti kwa onse kuti, Ndine citsiru. 4Ngati mkuru
akukwiyira, usasiye malo ako; cifukwa cifatso cipembedza
utacimwa kwambiri. 5Pali coipa ndaciona pansi pano, ngati
kulakwa koyambira ndi mkuru; 6utsiru ukhazikika pamwamba
penipeni, ndipo olemera angokhala mwamanyazi. 7Ndaona akapolo
atakwera pa akavalo, ndi mafumu, alikuyenda pansi ngati
akapolo. 8Wokumba mbuna adzagwamo; ndipo woboola mpanda
njoka idzamluma. 9Wosendeza miyala adzaphwetekedwa nayo;
wowaza nkhuni nadzitema. 10Citsulo cikakhala cosathwa, ndipo
ukaleka kunola, uzipambana kulimbikira; koma nzeru ipindulira
pocenjeza. 11Njoka ikaluma isanalodzedwe, watsenga saona
mphotho. 12Mau a m'kamwa mwa munthu wanzeru nga cisomo;
koma milomo ya citsiru idzacimeza. 13Ciyambi ca mau a m'kamwa
mwace ndi utsiru; ndipo cimariziro ca m'kamwa mwace ndi misala
yoipa, 14Citsiru cicurukitsanso mau; koma munthu sadziwa cimene
cidzaoneka; ndipo ndani angamuuze comwe cidzakhala m'tsogolo
mwace? 15Nchito ya zitsiru izitopetsa zonsezo, pakuti sicidziwa
kunka kumudzi. 16Tsoka kwa dzikowe, pamene mfumu yako ndiye
mwana, ndipo akalonga ako adyera mamawa! 17Mwai kwa
dzikowe, pamene mfumu yako ndiye mwana wa aufulu, ndipo
akalonga ako adya pa nthawi yoyenera akalimbe osati akaledzere
ai. 18Tsindwi litewa ndi mphwai za eni ace; nyumba nidontha ndi
ulesi wa manja. 19Amaphikira zakudya kuti asekere, vinyo
nakondweretsa moyo; ndipo ndalama zibvomera
zonse. 20Usatemberere mfumu ngakhale poganizira; usatemberere
wolemera m'cipinda cogona iwemo; pakuti mbalame ya
mlengalenga idzanyamula mauwo, ndipo couluka ndi mapiko
cidzamveketsa zonenazo.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Tizicita zokoma lero lino posadziwa za mawa

1Ponya zakudya zako pamadzi; udzazipeza popita masiku
ambiri. 2Gawira asanu ndi awiri ngakhale asanu ndi atatu; pakuti
sudziwa coipa canji cidzaoneka pansi pano. 3Mitambo ikadzala
mvula, itsanulira pansi; mtengo ukagwa kumwela pena kumpoto,
pomwe unagwa mtengowo udzakhala pomwepo. 4Woyang'ana
mphepo sadzafesa; ndi wopenya mitambo sadzakolola. 5Monga
sudziwa njira ya mphepo, ngakhale makulidwe a mafupa m'mimba
ya mkazi ali ndi pakati; momwemo sudziwa nchito za Mulungu
amene acita zonse. 6Mamawa fesa mbeu zako, madzulonso
osapumitsa dzanja lako; pakuti sudziwa ziti zidzalola bwino
ngakhale izizi, ngakhale izozo, kaya zonse ziwiri zidzakhala
bwino. 7Indetu kuunika nkokoma, maso napeza bwino m'kuona
dzuwa. 8Inde, munthu akakhala ndi moyo zaka zambiri, akondwere
ndi zonsezo; koma akumbukire masiku amdima kuti adzacuruka.
Zonse zirinkudza ziri zacabe.

Anyamata asangalale, koma adzikonzeretu pokumbukira imfa ikudza

9Kondwera ndi unyamata wako, mnyamata iwe; mtima wako
nukasangalale masiku a unyamata wako, nuyende m'njira za
mtima wako, ndi monga maso ako aona; koma dziwitsa kuti
Mulungu adzanena nawe mlandu wa zonsezi. 10Cifukwa cace
cotsani zopweteka m'mtima mwako, nulekanitse zoipa ndi thupi
lako; pakuti ubwana ndi unyamata ngwa cabe.

©The Bible Society of Malawi, 1992

1Ukumbukirenso Mlengi wako masiku a unyamata wako, asanadze
masiku oipa, ngakhale zisanayandikire zakazo zakuti udzati,
Sindikondwera nazo; 2ngakhale lisanade dzuwa, ndi kuunika, ndi
mwezi, ndi nyenyezi, mitambo ndi kubweranso italeka
mvula; 3tsikulo omwe asunga nyumba adzanthunthumira, amuna
olimba nadzawerama, akupera nadzaleka poperewera, omwe
ayang'ana pamazenera nadzadetsedwa; 4pa khomo lakunja
padzatsekeka; potsika mau akupera, wina nanyamuka polira
mbalame, ndipo akazi onse akuyimba sadzamveka bwino; 5inde,
adzaopa za pamwamba, panjira padzakhala zoopsya; mciu
nudzaphuka, dzombe ndi kukoka miyendo, zilakolako ndi kutha;
pakuti munthu apita kwao kwamuyaya, akulira maliro
nayendayenda panja; 6cingwe casiliva cisanaduke, ngakhale mbale
yagolidi isanasweke, ngakhale mtsuko usanaphwanyike kukasupe,
ngakhale njinga yotungira madzi isanatyoke kucitsime; 7pfumbi ndi
kubwera pansi pomwe linali kale, mzimu ndi kubwera kwa Mulungu
amene anaupereka. 8Cabe zacabetu, ati Mlalikiyo; zonse ndi cabe.

Zoyenera munthu ndizo kuopa Mulungu ndi kusunga malamulo ace

9Ndiponso pokhala wanzeru Mlalikiyo anaphunzitsabe anthu nzeru;
inde, anachera makutu nafunafuna
nalongosolamiyambiyambiri. 10Mlalikiyo anasanthula akapeze mau
okondweretsa, ndi zolemba zoongoka ngakhale mau oona.
11Mau a anzeru akunga zisonga, omwe akundika mau amene
mbusa mmodzi awapatsa mau ao akunga misomali yokhomedwa
zolimba. 12Pamodzi ndi izi, mwananga, tacenjezedwa; pakuti
saleka kulemba mabuku ambiri; ndipo kuphunzira kwambiri
kutopetsa thupi.
13Mau atha; zonse zamveka zatha; opa Mulungu, musunge
malamulo ace; pakuti coyenera anthu onse ndi ici. 14Pakuti
Mulungu adzanena mlandu wa zocita zonse, ndi zobisika zonse,
ngakhale zabwino ngakhale zoipa.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Song of songs

Nyimbo 1

Mkwatibwi anena ndi ana a Yerusalemu za mkwati

1NYIMBO yoposa, ndiyo ya Solomo.
2Mnyamatayo andipsompsonetse ndi m'kamwa mwace;
Pakuti cikondi cako ciposa vinyo.
3Mafuta ako anunkhira bwino;
Dzina lako likunga mafuta onunkhira otsanulidwa;
Cifukwa cace anamwali akukonda.
4Undikoke; tikuthamangire;
Mfumu yandilowetsa m'zipinda zace:
Tidzasangalala ndi kukondwera ndi iwe.
Tidzachula cikondi cako koposa vinyo:
Akukonda molungama.
5Wakuda ine, koma wokongola,
Ana akazinu a ku Yerusalemu,
Ngati mahema a Kedara,
Ngati nsaru zociriga za Solomo.
6Musayang'ane pa ine, pakuti ndada,
Pakuti dzuwa landidetsa.
Ana amuna a amai anandikwiyira,
Anandisungitsa minda yamipesa;
Koma munda wanga wanga wamipesa sindinausunga.
7Ndiuze, iwe amene moyo wanga ukukonda,
Umaweta kuti gulu lako?
Umaligonetsa kuti pakati pa usana?
Pakuti ndikhalirenji ngati wosocera
Pambali pa magulu a anzako?
8Ngati sudziwa, mkaziwe woposa kukongola,
Dzituruka kukalondola bande la gululo,
Nukawete ana a mbuzi zako pambali pa mahema a abusa.

Mkwati ndi mkwatibwi akambirana za cikondano cao

9Ndakulinganiza, wokondedwa wanga mnyamatawe,
Ngati akavalo a magareta a Farao.
10Masaya ako akongola ndi nkhata zatsitsi,
Ndi khosi lako ndi zinganga za mkanda wonyezimira.
11Tidzakupangira nkhata zagolidi
Ndi njumu zasiliva.
12Pokhala mfumu podyera pace,
Mphoka yanga inanunkhira.
13Wokondedwa wanga mnyamatayo ali kwa ine ngati thumba la nipa,
Logona pakati pa maere anga.

14Wokondedwa wanga ali kwa ine ngati cipukutu ca maluwa ofiira
M'minda yamipesa ya ku Engedi.
15Taona, wakongolatu, bwenzi langa; namwaliwe taona, wakongola,
Maso ako akunga a nkhunda.
16Taona, wakongolatu, bwenzi langa, mnyamatawe, inde,
wakongoletsa;
Pogona pathu mpa msipu.
17Mitanda ya nyumba zathu nja mikungudza,
Ndi mapaso athu nga mlombwa.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Nyimbo 2
1Ndine duwa lofiira la ku Saroni,
Ngakhale kakombo wa kuzigwa.
2Ngati kakombo pakati pa minga
Momwemo wokondedwa wanga pakati pa ana akazi.
3Ngati maula pakati pa mitengo ya m'nkhalango,
Momwemo wokondedwa wanga pakati pa ana amuna.
Ndinakondwa pakukhala pa mthunzi wace,
Zipatso zace zinatsekemera m'kamwa mwanga.
4Anandifikitsa ku nyumba ya vinyo,
Mbendera yace yondizolimira inali cikondi.
5Mundilimbikitse ndi mphesa zouma, munditonthoze mtima ndi maula,
Pakuti ndadwala ndi cikondi.
6Dzanja lace lamanzere anditsamiritse kumutu,
Dzanja lace lamanja ndi kundifungatira.
7Ndikulumbirirani, ana akazi inu a ku Yerusalemu,
Pali mphoyo, ndi nswala za kuthengo,
Kuti musautse, ngakhale kugalamutsa cikondi,
Mpaka cikafuna mwini.
8Mau a wokondedwa wanga mnyamatayo! Taona, adza,
Alikulumpha pamapiri, alikujidimuka pazitunda.
9Wokondedwa wanga akunga mphoyo, pena mwana wa mbawala:
Taona, aima patseri pa khoma pathu,
Apenyera pazenera, Nasuzumira pamade.
10Wokondedwa wanga analankhula, nati kwa ine,
Tauka, bwenzi langa, wokongola wanga, tiye.
11Pakuti, taona, cisanu catha,
Mvula yapita yaleka;
12Maluwa aoneka pansi;
Nthawi yoyimba mbalame yafika,
Mau a njiwa namveka m'dziko lathu;
13Mkuyu uchetsa nkhuyu zace zosakhwima,
Mipesa niphuka,
Inunkhira bwino.
Tauka, bwenzi langa, wokongola wangawe, tiyetu.
14Nkhunda yangawe, yokhala m'ming'alu ya thanthwe, mobisika motsetsereka,
Ndipenye nkhope yako, ndimve manako;
Pakuti mau ako ngokoma, nkhope yako ndi kukongola.
15Mutigwirire ankhandwe, ngakhale ang'ono, amene akuononga minda yamipesa;
Pakuti m'minda yathu yamipesa muphuka biriwiri.
16Wokondedwa wanga ndi wa ine, ine ndine wace:

Aweta zace pakati pa akakombo,
17Mpaka dzuwa litapepa, mithunzi ndi kutanimpha,
Bwera, bwenzi langawe, nukhale ngati mphoyo pena mwana wa mbawala
Pa mapiri a mipata.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Mkwatibwi apeza mkwati

1Usiku pamphasa panga ndinamfunafuna amene moyo wanga
umkonda:
Ndinamfunafuna, koma osampeza.
2Ndinati, Ndiuketu, ndiyendeyende m'mudzi,
M'makwalala ndi m'mabwalo ace,
Ndimfunefune amene moyo wanga umkonda:
Ndimfunafuna, koma osampeza.
3Alonda akuyendayenda m'mudzi anandipeza:
Ndinati, Kodi munamuona amene moyo wanga umkonda?
4Nditawapitirira pang'ono,
Ndinampeza amene moyo wanca umkonda:
Ndinamgwiriziza, osamfumbatula,
Mpaka nditamlowetsa m'nyumba ya amai,
Ngakhale m'cipinda ca wondibala.
5Ndikulumbirirani, ana akazi inu a ku Yerusalemu,
Pali mphoyo, ndi nswala ya kuthengo,
Kuti musautse, ngakhale kugalamutsa cikondi,
Mpaka cikafuna mwini.

Ulendo wa ukwati

6Ndaniyu akwera kuturuka m'cipululu ngati utsi wa tolo,
Wonunkhira ndi nipa ndi mtanthanyerere,
Ndi zonunkhiritsa zonse za wogulitsa?
7Taonani, ndi macila a Solomo;
Pazingapo amuna amphamvu makumi asanu ndi limodzi,
A mwa ngwazi za Israyeli.
8Onsewo agwira lupanga, nazolowera nkhondo:
Yense ali ndi lupanga lace pancafu pace,
Cifukwa ca upandu wa usiku.
9Solomo mfumu anadzipangira macila okhalamo tsonga
Ndi matabwa a ku Lebano.
10Anapanga timilongoti tace ndi siliva,
Ca pansi pace ndi golidi, mpando wace ndi nsaru yakuda,
Pakati pace panayalidwa za cikondi ca ana akazi a ku Yerusalemu.
11Turukani, ana akazi inu a Ziyoni, mupenye Solomo mfumu,
Ndi korona amace anambveka naye tsiku la ukwati wace,
Ngakhale tsiku lakukondwera mtima wace.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Nyimbo 4

Mkwati alemekeza mkwatibwi

1Taona, wakongola, bwenzi langa, namwaliwe, taona, wakongola;
Maso ako akunga a nkhunda patseri pa cophimba cako:
Tsitsi lako likunga gulu la mbuzi,
Zooneka pa phiri la Gileadi.
2Mano ako akunga gulu la nkhosa zosengasenga,
Zokwera kucokera kosamba;
Yonse iri ndi ana awiri,
Palibe imodzi yopoloza.
3Milomo yako ikunga mbota yofiira,
M'kamwa mwako ndi kukoma:
Palitsipa pako pakunga phande la khangaza
Patseri pa cophimba cako.
4Khosi lako likunga nsanja ya Davide anaimangira zida,
Apacikapo zikopa zikwi,
Ngakhale zikopa zonse za amuna amphamvu,
5Maere ako awiri akunga ana awiri a nswala obadwa limodzi,
Akudya pakati pa akakombo.
6Mpaka dzuwa litapepa, mithunzi ndi kutanimpha,
Ndikamuka ku phiri la nipa,
Ndi ku citunda ca mtanthanyerere.
7Wakongola monse monse, wokondedwa wanga, namwaliwe,
Mulibe cirema mwa iwe.
8Idza nane kucokera ku Lebano, mkwatibwi,
Kucokera nane ku Lebano:
Unguza pamwamba pa Amana,
Pa nsonga ya Seniri ndi Hermoni,
Pa ngaka za mikango,
Pa mapiri a anyalugwe.
9Walanda mtima wanga, mlongwanga, mkwatibwi;
Walanda mtima wanga ndi diso lako limodzi,
Ndi cinganga cimodzi ca pakhosi pako,
10Ha, cikondi cako ncokongola, mlongwanga, mkwatibwi!
Kodi cikondi cako siciposa vinyo?
Kununkhira kwa mphoka yako ndi kuposa zonunkhiritsa za mitundu mitundu!
11M'milomo yako, mkwatibwi, mukukha uci,
Uci ndi mkaka ziri pansi pa lilime lako;
Kununkhira kwa zobvala zako ndi kunga kununkhira kwa Lebano,
12Mlongwanga, mkwatibwi ndiye munda wotsekedwa;
Ngati kasupe wotsekedwa, ndi citsime copikiza.
13Mphukira zako ndi munda wamakangaza,
Ndi zipatso zofunika, bononwe ndi mphoka,

14Mphoka ndi cikasu,
Nzimbe ndi ngaho, ndi mitengo yonse yamtanthanyerere;
Nipa ndi khonje, ndi zonunkhiritsa zonse zomveka.
15Ndiwe kasupe wa m'minda,
Citsime ca madzi amoyo,
Ndi mitsinje yoyenda yocokera ku Lebano.

Ayankha mkwatibwi

16Galamuka, mphepo ya kumpoto iwe, nudze, mphepo iwe ya kumwela;
Nuombe pamunda panga, kuti zonunkhiritsa zace ziturukemo.
Bwenzi langa mnyamatayo, alowe m'munda mwace,
Nadye zipatso zace zofunika.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Nyimbo 5
1Ndalowa m'munda mwanga, mlongwanga, mkwatibwi:
Ndachera nipa yanga ndi zonunkhiritsa zanga;
Ndadya uci wanga ndi cisa cace;
Ndamwa vinyo wanga ndi mkaka wanga.
Idyani, atsamwalinu,
Imwani, mwetsani cikondi.
Alekana nthawi
2Ndinagona tulo, koma mtima wanga unali maso:
Ndi mau a bwenzi langa mnyamatayo agogoda, nati,
Nditsegulire, mlongwanga, wokondedwa wanga, nkhunda yanga, wangwiro wanga:
Pakuti pamtu panga padzala mame,
Patsitsi panga pali madontho a usiku.
3Ndinayankha kuti, Ndabvula maraya anga, ndiwabvalenso bwanji?
Ndatsuka mapazi anga; ndiwadetserenii?
4Bwenzi langa analonga dzanja lace pazenera,
Mtima wanga ndi kuguguda cifukwa ca iye,
5Ndinauka ndikatsegulire bwenzi langa;
Pamanja panga panakha nipa.
Ndi pa zala zanga madzi a nipa, Pa zogwirira za mpikizo,
6Ndinamtsegulira bwenzi langalo;
Koma ndinampeza, bwenzi langa atacoka.
Moyo wanga unalefuka polankhula iye:
Ndinamfunafuna, osampeza;
Ndinamuitana, koma sanandibvomera.
7Alonda akuyenda m'mudzi anandipeza,
Nandikantha, nanditema;
Osunga maguta nandicotsera cophimba canga.
8Ndikulumbirirani, ana akazi inu a ku Yerusalemu,
Mukapeza bwenzi langa, mudzamuuza ciani?
Kuti ndadwala ndi cikondi.
9Bwenzi lako aposa abwenzi ena bwanji,
Mkaziwe woposa kukongola?
Bwenzi lako aposa abwenzi ena bwanji,
Kuti utilumbirira motero?
10Wokondedwa wanga ali woyera ndi wofiira,
Womveka mwa zikwi khumi.
11Mutu wace ukunga golidi, woyengetsa,
Tsitsi lace lopotana, ndi lakuda ngati khungubwi.
12Ana a maso ace akunga nkhunda pambali pa mitsinje ya madzi;
Otsukidwa ndi mkaka, okhala pa mitsinje yodzala.
13Masaya ace akunga citipula cabzyalamo ndiwo,
Ngati mitumbira yoyangapo masamba onunkhira:

Milomo yace ikunga akakombo, pakukhapo madzi a nipa.
14Manja ace akunga zing'anda zagolidi zoikamo zonyezimira zoti
biriwiri:
Thupi lace likunga copanga ca minyanga colemberapo masafiro.
15Miyendo yace ikunga zoimiritsa za mwala wonyezimira,
Zogwirika m'kamwa mwa golidi:
Maonekedwe ace akunga Lebano, okometsetsa ngati mikungudza.
16M'kamwa mwace muli mokoma: inde, ndiye wokondweretsa
ndithu.
Ameneyu ndi wokondedwa wanga, ameneyu ndi bwenzi langa,
Ana akazi inu a ku Yerusalemu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

1Bwenzi lako wapita kuti,
Mkaziwe woposa kukongola?
Bwenzi lako wapambukira kuti,
Tikamfunefune pamodzi nawe?
2Bwenzi langa watsikira kumunda kwace,
Ku zitipula za mphoka, Kukadya kumunda kwace, ndi kuchera akakombo.
3Ndine wace wa wokondedwa wanga, wokondedwa wanganso ndiye wa ine;
Aweta zace pakati pa akakombo.
Mkwati ndi mkwatibwi alemekezana
4Wakongola, bwenzi langa, namwaliwe ngati Tiriza,
Wokoma ngati Yerusalemu,
Woopsya ngati nkhondo ndi mbendera.
5Undipambutsire maso ako, Pakuti andiopetsa.
Tsitsi lako likunga gulu la mbuzi,
Zigona pambali pa Gileadi.
6Mano ako akunga gulu la nkhosa zazikazi,
Zikwera kucokera kosamba; Yonse iri ndi ana awiri,
Palibe imodzi yopoloza.
7Palitsipa pako pakunga phande la khangaza
Patseri pa cophimba cako.
8Alipo akazi akulu a mfumu makumi asanu ndi limodzi,
Kudza akazi ang'ono makumi asanu ndi atatu,
Ndi anamwali osawerengeka.
9Nkhunda yanga, wangwiro wangayu, ndiye mmodzi;
Ndiye wobadwa yekha wa amace;
Ndiye wosankhika wa wombala.
Ana akazi anamuona, namucha wodala;
Ngakhale akazi akulu a mfumu, ndi akazi ang'ono namtamanda.
10Nati, Ndaniyo aturuka ngati mbanda kuca,
Wokongola ngati mwezi,
Woyera ngati dzuwa,
Woopsya ngati nkhondo ndi mbendera?
11Ndinatsikira ku munda wa ntedza,
Kukapenya msipu wa m'cigwa,
Kukapenya ngati pamipesa paphuka,
Ngati pamakangaza patuwa maluwa.
12Ndisanazindikire, moyo wanga unandiimika
Pakati pa magareta a anthu anga aufulu.
13Anati, Bwera, bwera, Msulamiwe;
Bwera, bwera, tiyang'ane pa iwe.
Muyang'aniranji pa Msulami,

Ngati pa masewero akuguba?

©The Bible Society of Malawi, 1992

Nyimbo 7

1Ha, mapazi ako akongola m'zikwakwata,
Mwana wamkaziwe wa mfumu!
Pozinga m'cuuno mwako pakunga zonyezimira,
Nchito ya manja a mmisiri waluso.
2Pamcombo pako pakunga cikho coulungika,
Cosasowamo vinyo wosanganika:
Pamimba pako pakunga mulu wa tirigu
Wozingidwa ndi akakombo.
3Maere ako akunga ana awiri a nswala
Anabadwa limodzi.
4Khosi lako likunga nsanja yaminyanga;
Maso ako akunga matawale a ku Hesiboni,
A pa cipata ca Batirabimu;
Mphuno yako ikunga nsanja ya ku Lebano
Imene iloza ku Damasiko.
5Mutu wako ukunga Karimeli,
Ndi tsitsi la pamtu pako likunga nsaru yakuda;
Mfumu yamangidwa ndi nkhata zace ngati wamsinga.
6Ha, ndiwe wokongola ndi wofunika,
Bwenziwe, m'zokondweretsa!
7Msinkhu wakowu ukunga mlaza,
Maere ako akunga matsango amphesa,
8Ndinati, Ndikakwera pamlazapo,
Ndikagwira nthambi zace:
Maere ako ange ngati matsango amphesa,
Ndi kununkhira kwa mpweya wako ngati maula;
9M'kamwa mwako munge ngati vinyo woposa,
Womeza tseketeke bwenzi langa,
Wolankhulitsa milomo ya ogona tulo.
10Ndine wa wokondedwa wanga mnyamatayo,
Ndine amene andifunayo.
11Tiye, bwenzi langa, tinke kuminda;
Titsotse m'miraga.
12Tilawire kunka ku minda yamipesa;
Tiyang'ane ngati mpesa waphuka, kunje ndi kuonetsa zipatso,
Makangaza ndi kutuwa maluwa ace;
Pompo ndidzakupatsa cikondi canga,
13Mandimu anunkhira,
Ndi pamakomo pathu zipatso zabwino, za mitundu mitundu, zakale ndi zatsopano,
Zimene ndakukundikira iwe, wokondedwa wanga.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Nyimbo 8
1Mwenzi utakhala ngati mlongwanga,
Woyamwa pa bere la amai!
Ndikadakupeza panja, ndikadakupsompsona;
Osandinyoza munthu.
2Ndikadakutsogolera, kukulowetsa m'nyumba ya amai,
Kuti andilange mwambo; Ndikadakumwetsa vinyo wokoleretsa,
Ndi madzi a makangaza anga.
3Dzanja lamanzere lace akadanditsamiritsa kumutu,
Lamanja lace ndi kundifungatira.
4Ndikulumbirirani, ana akazi inu a ku Yerusalemu,
Muutsiranji, mugalamutsiranji cikondi,
Cisanafune mwini.
5Ndaniyu acokera kucipululu,
Alikutsamira bwenzi lace?
Pa tsinde la muula ndinakugalamutsa mnyamatawe:
Pomwepo amako anali mkusauka nawe,
Pomwepo wakukubala anali m'pakati pa iwe.
6Undilembe pamtima pako, mokhoma cizindikilo, nundikhomenso cizindikilo pamkono pako;
Pakuti cikondi cilimba ngati imfa;
Njiru imangouma ngati manda:
Kung'anima kwace ndi kung'anima kwa moto,
Ngati mphezi ya Yehova,
7Madzi ambiri sangazimitse cikondi,
Ngakhale mitsinje yodzala kucikokolola:
Mwamuna akapereka katundu yense wa m'nyumba yace ngati sintho la cikondi,
Akanyozedwa ndithu.
8Tiri ndi mlongwathu wamng'ono,
Alibe maere;
Ticitirenji mlongwathu
Tsiku lokhoma unkhoswe wace?
9Ngati ndiye khoma, tidzamanga pa iye nsanja yasiliva:
Ngati ndiye citseko tidzamtsekereza ndi matabwa amikungudza.
10Ndine khoma, maere anga akunga nsanja zace:
Pamaso pa mnyamatayo ndinafanana ngati wopeza mtendere.
11Solomo anali ndi munda wamipesa ku Baalahamoni;
Nabwereka alimi mundawo;
Yense ambwezere ndalama cikwi cifukwa ca zipatso zace.
12Koma munda wanga wamipesa, uli pamaso panga ndiwo wangatu;
Naco cikwico, Solomo iwe,
Koma olima zipatso zace azilandira mazana awiri.

13Namwaliwe wokhala m'minda,
Anzake amvera mau ako:
Nanenso undimvetse.
14Dzifulumira, mnyamatawe wokondedwa wanga,
Dzifanane ngati mphoyo pena mwana wa mbawala
Pa mapiri a mphoka,

©The Bible Society of Malawi, 1992

Isaiah

Yesaya 1

Macimo ndi masauko a ana a Israyeli

1MASOMPHENYA a Yesaya mwana wa Amozi, amene iye anaona,
onena za Yuda ndi Yerusalemu, masiku a Uziya, Yotamu, Ahazi, ndi
Hezekiya, mafumu a Yuda.
2Imvani, miyamba inu, chera makutu, iwe dziko lapansi, cifukwa
Yehova wanena, Ndakulitsa ndipo ndalera ana, ndipo iwo
anandipandukira Ine. 3Ng'ombe idziwa mwini wace, ndi buru
adziwa pomtsekereza: koma Israyeli sadziwa, anthu anga
sazindikira. 4Mtundu wocimwa inu, anthu olemedwa ndi
mphulupulu, mbeu yakucita zoipa, ana amene acita moononga,
iwo amsiya Yehova, iwo amnyoza Woyera wa Israyeli, iwo adana
naye nabwerera m'mbuyo. 5Nanga bwanji mukali cimenyedwere
kuti inu mulikupandukirabe? Mutu wonse ulikudwala, ndi mtima
wonse walefuka. 6Kucokera pansi pa phazi kufikira kumutu
m'menemo mulibe cangwiro; koma mabala, ndi mikwingwirima,
ndi zironda; sizinapole, ngakhale kumangidwa, ngakhale
kupakidwa mafuta. 7Dziko lanu liri bwinja; midzi yanu yatenthedwa
ndi moto; dziko lanu alendo alimkudya pamaso panu; ndipo liri
labwinja monga lagubuduzidwa ndi alendo. 8Ndipo mwana
wamkazi wa Ziyoni wasiyidwa ngati citando ca m'munda
wamphesa, ngati cilindo ca m'munda wamankhaka, ngati mudzi
wozingidwa ndi nkhondo. 9Akadapanda Yehova wa makamu
kutisiyira otsala ang'onong'ono ndithu, ife tikanakhala ngati
Sodomu, ife tikadanga Gomora.

Macenjezo ndi maopso a Mulungu

10Imvani mau a Yehova inu olamulira a Sodomu, cherani makutu ku
cilamulo ca Mulungu wathu, inu anthu a Gomora. 11Nditani nazo
nsembe zanu zocurukazo? ati Yehova; ndakhuta nazo nsembe
zopsereza za nkhosa zamphongo ndi mafuta a nyama zonenepa;
sindisekera ndi mwazi wa ng'ombe zamphongo, ngakhale wa ana a
nkhosa, ngakhale wa atonde. 12Pakudzaonekera inu pamaso pa
Ine, ndani wafuna cimeneci m'dzanja lanu, kupondaponda
m'mabwalo mwanga? 13Musadze nazonso, nsembe zacabecabe;
nsembe zofukiza zindinyansa; tsiku lokhala mwezi ndi sabata,
kumema masonkhano, sindingalole mphulupulu ndi
masonkhano. 14Masiku anu okhala mwezi ndi nthawi za mapwando
anu mtima wanga uzida; zindibvuta Ine; ndalema ndi kupirira
nazo. 15Ndipo pamene mutambasula manja anu, ndidzakubisirani
inu maso anga; inde pocurukitsa mapemphero anu Ine
sindidzamva; manja anu adzala mwazi. 16Sambani, dziyeretseni;
cotsani macitidwe anu oipa pamaso panga; lekani kucita

zoipa; 17phunzirani kucita zabwino; funani ciweruzo; thandizani
osautsidwa, weruzirani ana amasiye, munenere akazi amasiye.
18Tiyeni, tsono, tiweruzane, ati Yehova; ngakhale zoipa zanu ziri
zofiira, zidzayera ngati matalala; ngakhale ziri zofiira ngati kapezi,
zidzakhala ngati ubweya wa nkhosa, woti mbu. 19Ngati inu muli
ofuna ndi omvera, mudzadya zabwino za dziko, 20koma ngati
mukana ndi kupanduka, mudzathedwa ndi lupanga; cifukwa
m'kamwa mwa Yehova mwatero.
21Mudzi wokhulupirika wasanduka wadama! wodzala ciweruzowo!
cilungamo cinakhalamo koma tsopano ambanda. 22Siliva wako
wasanduka mphala, vinyo wako wasanganizidwa ndi
madzi. 23Akuru ako apanduka, ali anzao a mbala; onse akonda
mitulo, natsata zokometsera mirandu; iwo saweruzira amasiye;
ngakhale mlandu wa mkazi wamasiye suwafika.
24Cifukwa cace Yehova ati, Yehova wa makamu wamphamvu wa
Israyeli, Ha! ndidzatonthoza mtima wanga pocotsa ondibvuta, ndi
kubwezera cilango adani anga; 25ndipo ndidzaikanso dzanja langa
pa iwe, ndi kukusungunula kukusiyanitsa iwe ndi mphala yako,
ndipo ndidzacotsa seta wako wonse: 26ndidzabweza oweruza ako
monga poyamba, ndi aphungu ako monga paciyambi; pambuyo
pace udzachedwa Mudzi wolungama, mudzi
wokhulupirika. 27Ziyoni adzaomboledwa ndi ciweruzo, ndi
otembenuka mtima ace ndi cilungamo. 28Koma kupasula kwa
olakwa ndi kwa ocimwa kudzakhala kumodzi, ndi iwo amene asiya
Yehova adzathedwa. 29Cifukwa adzakhala ndi manyazi, cifukwa ca
mitengo yathundu munaikhumba, ndipo inu mudzagwa nkhope,
cifukwa ca minda imene mwaisankha. 30Cifukwa mudzakhala ngati
mtengo wathundu, umene tsamba lace linyala, ngatinso munda
wopanda madzi. 31Ndimo wamphamvu adzakhala ngati cingwe
cabwazi, ndi nchito yace ngati nthethe; ndipo zonse zidzayaka
moto pamodzi, opanda wozimitsa.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Ulemerero wa Israyeli m'tsogolomo, maweruzo a Mulungu pakatipo

1Mau amene Yesaya mwana wa Amozi anaona, onena za Yuda ndi
Yerusalemu.
2Ndipo padzakhala masiku otsiriza, kuti phiri la nyumba ya Yehova
lidzakhazikika pa nsonga ya mapiri, ndipo lidzakwezedwa
pamwamba pa zitunda; mitundu yonse idzasonkhana
kumeneko. 3Ndipo anthu ambiri adzanka, nati, Tiyeni tikwere
kunka ku phiri la Yehova, ku nyumba ya Mulungu wa Yakobo; ndipo
Iye adzatiphunzitsa za njira zace, ndipo tidzayenda
m'mayendedwe ace; cifukwa m'Ziyoni mudzaturuka cilamulo, ndi
mau a Yehova kucokera m'Yerusalemu. 4Iye adzaweruza pakati pa
akunja, adzadzudzula mitundu yambiri ya anthu; ndipo iwo
adzasula malupanga ao akhale zolimira, ndi nthungo zao zikhale
anangwape; mtundu sudzanyamula lupanga kumenyana ndi
mtundu wina, ndipo sadzaphunziranso nkhondo.
5Inu a nyumba ya Yakobo, tiyeni, tiyende m'kuwala kwa
Yehova. 6Cifukwa inu mwasiya anthu anu a nyumba ya Yakobo,
cifukwa kuti iwo adzazidwa ndi miyambo ya kum'mawa, ndipo ali
olaula ngati Afilisti, naomba m'manja ndi ana a acilendo. 7Dziko lao
ladzala siliva ndi golidi, ngakhale cuma cao ncosawerengeka; dziko
lao lidzalanso akavalo, ngakhale magareta ao
ngosawerengeka. 8Dziko lao ladzalanso mafano; iwo apembedza
nchito ya manja ao ao, imene zala zao zao zinaipanga. 9Munthu
wacabe agwada pansi, ndi munthu wamkuru adzicepetsa, koma
musawakhululukire. 10Lowa m'phanga, bisala m'pfumbi, kucokera
pa kuopsya kwa Yehova, ndi pa ulemerero wacifumu wace. 11Maso
a munthu akuyang'anira kumwamba adzatsitsidwa, ndi kudzikweza
kwa anthu kudzaweramitsidwa pansi; ndipo Yehova yekha
adzakwezedwa tsiku limenelo. 12Cifukwa padzakhala tsiku la
Yehova wa makamu pa zonse zonyada ndi zakudzikuza, ndi pa
zonse zotukulidwa; ndipo zidzatsitsidwa; 13ndi pa mitengo yonse
yamkungudza ya Lebano, yaitari ndi yotukulidwa, ndi pa mitengo
yonse yathundu ya Basana; 14ndi pa mapiri onse atari, ndi pa
zitunda zonse zotukulidwa; 15ndi pa nsanja zazitari zonse, ndi pa
macemba onse; 16ndi pa ngalawa zonse za Tarisi, ndi pa
zithunzithunzi zonse zokondweretsa. 17Ndipo kudzikweza kwa
munthu kudzaweramitsidwa pansi, kudzikuza kwa munthu
kudzatsitsidwa; ndipo Yehova yekha adzakwezedwa tsiku
limenelo. 18Ndimo mafano adzapita psiti. 19Anthu adzalowa
m'mapanga a m'matanthwe, ndi m'maenje apansi, kuthawa
kuopsya kwa Yehova, ndi ulemerero wacifumu wace, podzuka Iye
kugwedeza dziko ndi mphamvu. 20Tsiku limenelo munthu adzataya

ku mfuko ndi ku mileme mafano ace asiliva ndi agolidi amene
anthu anampangira iye awapembedze; 21kuti akalowe m'mapanga
a m'matanthwe, ndi m'mindala a m'miyala, kuthawa kuopsya kwa
Yehova, ndi ulemerero wacifumu wace, podzuka Iye kugwedeza
dziko ndi mphamvu, 22Siyani munthu, amene mpweya wace uli
m'mphuno mwace; cifukwa m'mene awerengedwamo ndi muti?

©The Bible Society of Malawi, 1992

1Ndipo onani, Ambuye, Yehova wa makamu, wacotsa ku Yerusalemu
ndi ku Yuda mcirikizo wocirikiza cakudya conse ndi madzi onse,
zimene zinali mcirikizo; 2munthu wamphamvu, ndi munthu
wankhondo; woweruza, ndi mneneri, ndi waula, ndi
nkhalamba; 3kapitao wa makumi asanu, ndi munthu wolemekezeka,
ndi mphungu, ndi mmisiri waluso, ndi wodziwa matsenga. 4Ndipo
ndidzapereka ana, kuti akhale akuru ao, mwacibwana
adzawalamulira. 5Ndi anthu adzabvutidwa, yense ndi wina, yense
ndi mnansi wace; mwana adzadzinyaditsa yekha pa akuru, ndi
onyozeka pa olemekezedwa. 6Pamene mwamuna adzamgwira
mbale wace m'nyumba ya atate wace, nadzati, Iwe uli ndi cobvala,
khala wolamulira wathu, ndi kupasula kumeneku kukhale m'dzanja
lako; 7tsiku limenelo adzakweza mau ace, kuti, Sindine wociritsa,
cifukwa kuti m'nyumba mwanga mulibe cakudya kapena cobvala;
inu simudzandiyesa ine wolamulira anthu. 8Cifukwa kuti Yerusalemu
wapasulidwa, ndi Yuda wagwa; cifukwa kuti lilume lao ndi macitidwe
ao akana Yehova, kuti autse mkwiyo wa m'maso a ulemerero
wace. 9Maonekedwe a nkhope zao awacitira iwo mboni; ndipo
amaonetsa ucimo wao monga Sodomu, saubisa. Tsoka kwa moyo
wao! cifukwa iwo anadzicitira zoipa iwo okha. 10Nenani za
wolungama, kuti kudzamkomera iye; cifukwa oterowo adzadya
zipatso za macitidwe ao. 11Tsoka kwa woipa! kudzamuipira; cifukwa
kuti mphotho ya manja ace idzapatsidwa kwa iye. 12Anthu anga
awabvuta ndi ana, awalamulira ndi akazi. Anthu anga inu, iwo
amene akutsogolerani, ndiwo akucimwitsani, naononga njira zanu
zoyendamo. 13Yehova aimirira kuti atsutsane, naimiriranso kuti
aweruze mitundu ya anthu. 14Yehova adzalowa monenera mirandu
ndi okalamba a anthu ace, ndi akuru ace: Ndinu amene mwadya
munda wamphesa, zofunkha za waumphawi ziri m'nyumba
zanu; 15muti bwanji inu, amene mupsinja anthu anga, ndi kupera
nkhope ya wosauka? ati Ambuye Yehova wa makamu.
16Komanso Yehova ati, Cifukwa kuti ana akazi a Ziyoni angodzikuza
atakweza makosi ao, ndi maso ao adama nayenda nanyang'ama
poyenda pao naliza zigwinjiri za mapazi ao; 17cifukwa cace
Ambuye adzacita nkanambo pa liwombo la ana akazi a Ziyoni,
ndipo Yehova adzabvundukula m'cuuno mwao. 18Tsiku limenelo
Ambuye adzacotsa zigwinjiri zao zokoma, ndi zitunga, ndi
mphande; 19mbera, ndi makoza, ndi nsaru za pankhope; 20ndi
zisada, ndi maunyolo a kumwendo, ndi mipango, ndi nsupa
zonunkhira, ndi mphinjiri; 21mphete, ndi zipini; 22malaya a
paphwando, ndi zopfunda, ndi zimbwi, ndi timatumba; 23akalirole,
ndi nsaru zabafuta, ndi nduwira, ndi zophimba. 24Ndipo padzakhala
m'malo mwa zotsekemera mudzakhala zobvunda; ndi m'malo mwa

lamba cingwe; ndipo m'malo mwa tsitsi labwino dazi; m'malo mwa
cobvala ca pacifuwa mpango waciguduli; zipsera m'malo mwa
ukoma. 25Amuna ako adzagwa ndi lupanga, ndi wamphamvu wako
m'nkhondo. 26Ndipo zipata zace zidzalira maiko; ndipo iye
adzakhala bwinja, nadzakhala pansi.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Tsiku la Mulungu, kuyeretsedwa kwa Yerusalemu

1Ndipo akazi asanu ndi awiri adzagwira mwamuna mmodzi tsiku
limenelo, nati, Ife tidzadya cakudya cathu cathu ndi kubvala
zobvala zathu zathu; koma tichedwe dzina lako; cotsa citonzo
cathu.
2Tsiku limenelo mphukira ya Yehova idzakhala yokongola ndi ya
ulemerero, cipatso ca nthaka cidzakhala cokometsetsa ndi
cokongola, kwa iwo amene adzapulumuka a Israyeli. 3Ndipo
padzakhala, kuti iye amene asiyidwa m'Ziyoni, ndi iye amene
atsala m'Yerusalemu, adzachedwa woyera; ngakhale yense amene
walembedwa mwa amoyo m'Yerusalemu; 4pamene Ambuye
adzasambitsa litsiro la ana akazi a Ziyoni, nadzatsuka mwazi wa
Yerusalemu, kucokera pakatipo, ndi mzimu wa ciweruziro, ndi
mzimu wakutentha. 5Ndipo Yehova adzalenga pokhala ponse pa
phiri la Ziyoni, ndi pa masonkhano ace, mtambo ndi utsi usana, ndi
kung'azimira kwa malawi a moto usiku; cifukwa kuti pa ulemerero
wonse padzayalidwa cophimba. 6Ndipo padzakhala cihema ca
mthunzi, nthawi ya usana yopewera kutentha, pothawira ndi pousa
mvula ndi mphepo.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Fanizo la munda wamphesa ndi kumasulira kwace

1Ndiyimbire wokondedwa wanga nyimbo ya wokondedwa wanga
ya munda wace wamphesa, Wokondedwa wanga anali ndi munda
wamphesa m'citunda ca zipatso zambiri; 2ndipo iye anakumba
mcerenje kuzungulira kwete, natolatola miyala pamenepo naokapo
mpesa wosankhika, namangapo pakati pace nsanja, nasema
mopondera mphesa, nayembekeza kuti udzabala mphesa, koma
unangobala mphesa zosadya. 3Ndipo tsopano, inu okhala
m'Yerusalemu, ndi anthu a Yuda, weruzanitu mlandu wa ine ndi
munda wanga wamphesa. 4Ndikanacitanso ciani ndi munda wanga
wamphesa, cimene sindinacite m'menemo; muja ndinayembekeza
kuti udzabala mphesa, wabaliranji mphesa zosadya? 5Ndipo
tsopano ndidzakuuzani cimene nditi ndicite ndi munda wanga
wamphesa; ndidzacotsapo chinga lace, ndipo zidzadyedwa;
ndidzagumula linga lace, ndipo zidzapondedwa pansi; 6ndipo
ndidzaupasula; sudzadzomboleredwa kapena kulimidwa; koma
padzamera lunguzi ndi minga; ndidzalamuliranso mitambo kuti
isabvumbwepo mvula. 7Cifukwa kuti munda wamphesa wa Yehova
wa makamu ndiwo banja la Israyeli, ndi anthu a Yuda, mtengo
wace womkondweretsa; Iye anayembekeza ciweruziro, koma onani
kuphana; nayembekeza cilungamo, koma onani kupfuula.
8Tsoka kwa iwo amene aphatikiza nyumba ndi nyumba, amene
alumikiza munda ndi munda, kufikira padzapanda malo, ndipo inu
mudzasiyidwa nokha pakati pa dziko! 9M'makutu anga, ati Yehova
wa makamu, Zoonadi nyumba zambiri zidzakhala bwinja, ngakhale
zazikuru ndi zokoma zopanda wokhalamo. 10Cifukwa kuti munda
wamphesa wa madera khumi udzangobala mbiya imodzi, ndi
mbeu za nsengwa khumi zidzangobala nsengwa imodzi.
11Tsoka kwa iwo amene adzuka m'mamawa kuti atsate zakumwa
zaukali; amene acezera usiku kufikira vinyo awaledzeretsal 12Ndipo
zeze ndi mgoli, ndi lingaka ndi citoliro, ndi vinyo, ziri m'mapwando
ao; koma iwo sapenyetsa nchito ya Yehova; ngakhale kuyang'ana
pa macitidwe a manja ace. 13Cifukwa cace anthu anga amuka
m'nsinga, cifukwa ca kusowa nzeru; ndi amuna ao olemekezeka ali
ndi njala, ndi khamu lao lauma kukhosi. 14Ndipo manda akuza
cilakolako cace, natsegula kukamwa kwace kosayeseka; ndi
ulemerero wao, ndi unyinji wao, ndi phokoso lao, ndi iye amene
akondwerera mwa iwo atsikira mommo. 15Munthu wonyozeka
waweramitsidwa, ndi munthu wochuka watsitsidwa, ndi maso a
wodzikweza atsitsidwa; 16koma Yehova wa makamu wakwezedwa
m'ciweruziro, ndipo Mulungu Woyera wayeretsedwa
m'cilungamo. 17Pamenepo ana a nkhosa adzadyapo ngati m'busa
mwao, ndi malo a bwinja a zonenepa zacilendo zidzadyapo.

18Tsoka kwa iwo amene akoka mphulupulu ndi zingwe zacabe, ndi
cimo ngati ndi cingwe ca gareta; 19amene ati, Mlekeni iye
akangaze, mlekeni iye afulumize nchito yace kuti ife tione; ndipo
lekani uphungu wa Woyera wa Israyeli uyandikire, udze kuti
tiudziwe!
20Tsoka kwa iwo amene ayesa zoipa zabwino, ndi zabwino zoipa;
amene aika mdima m'malo mwa kuyera, ndi kuyera m'malo mwa
mdima; amene aika zowawa m'malo mwa zotsekemera, ndi
zotsekemera m'malo mwa zowawa!
21Tsoka kwa iwo amene adziyesera anzeru ndi ocenjera!
22Tsoka kwa iwo amene ali a mphamvu yakumwa vinyo, ndi anthu
olimba akusanganiza zakumwa zaukali; 23amene alungamitsa
woipa pa cokometsera mlandu, nacotsera wolungama cilungamo
cace! 24Cifukwa cace monga ngati lilime la moto likutha ciputu, ndi
monga udzu wouma ugwa pansi m'malawi, momwemo muzu wao
udzakhala monga wobvunda, maluwa ao adzauluka m'mwamba
ngati pfumbi; cifukwa kuti iwo akana cilamulo ca Yehova wa
makamu, nanyoza mau a Woyera wa Israyeli.
25Cifukwa cace mkwiyo wa Yehova wayaka pa anthu ace, ndipo Iye
watambasulira iwo dzanja lace, nawakantha, ndipo zitunda
zinanthunthumira, ndi mitembo yao inali ngati zinyatsi pakati pa
makwalala. Mwa izi zonse mkwiyo wace sunacoke, koma dzanja
lace liri citambasulire. 26Ndipo Iye adzakwezera a mitundu yakutari
mbendera, nadzawayimbira mluzu, acokere ku malekezero a dziko;
ndipo taonani, iwo adzadza ndi liwiro msanga msanga; 27palibe
amene adzalema, kapena adzapunthwa mwa iwo, palibe amene
adzaodzera kapena kugona tulo; ngakhale lamba la m'cuuno mwao
silidzamasuka, kapena comangira ca nsapato zao
sicidzaduka; 28amene mibvi yao ili yakuthwa, ndi mauta ao onse
athifuka; ziboda za akavalo ao zidzayesedwa ngati mwala, ndi
njinga zao ngati kabvumvulu; 29kubangula kwao kudzafana ndi
mkango, iwo adzabangula ngati ana a mikango, inde iwo
adzabangula, nadzagwira nyama, naicotsa bwino opanda
wakupulumutsa. 30Ndipo iwo adzawabangulira tsiku limenelo ngati
kukokoma kwa nyanja; ndipo wina ayang'ana padziko, taonani
mdima ndi nsautso, kuyera kwadetsedwanso m'mitambo yace.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masomphenya a Yesaya

1Caka cimene mfumu Uziya anafa, ndinaona Ambuye atakhala pa
mpando wacifumu wautari, ndi wotukulidwa, ndi zobvala zace
zinadzala m'Kacisi. 2Pamwamba pa Iye panaima aserafi; yense
anali ndi mapiko asanu ndi limodzi; awiri anaphimba nao nkhope
yace, awiri naphimba nao mapazi ace, awiri nauluka nao. 3Ndipo
wina anapfuula kwa mnzace, nati, Woyera, Woyera, Woyera,
Yehova wa makamu; dziko lonse lapansi ladzala ulemerero
wace. 4Ndipo maziko a ziundo anasunthika ndi mau amene
anapfuula, ndipo nyumba inadzazidwa ndi utsi. 5Ndipo ine ndinati,
Tsoka kwa ine! cifukwa ndathedwa; cifukwa ndiri munthu wa
milomo yonyansa, ndikhala pakati pa anthu a milomo yonyansa;
cifukwa kuti maso anga aona Mfumu, Yehova wa makamu.

Yesaya akonzedwa akhale mneneri

6Pompo anaulukira kwa ine mmodzi wa aserafi, ali nalo khala
lamoto m'dzanja mwace, limene analicotsa ndi mbaniro pa guwa la
nsembe; 7nakhudza nalo kukamwa kwanga nati, Taona ici
cakhudza milomo yako; ndipo mphulupulu zako zacotsedwa,
zocimwa zako zaomboledwa. 8Ndipo ndinamva mau a Ambuye
akuti, Ndidzatumiza yani, ndipo ndani adzatimukira ife? Ndipo ine
ndinati, Ndine pano; munditumize ine. 9Ndipo Iye anati, Kauze
anthu awa, Imvani inu ndithu, koma osazindikira; yang'anani inu
ndithu, koma osadziwitsa. 10Nenepetsa mtima wa anthu awa,
lemeretsa makutu ao, nutseke maso ao; angaone ndi maso ao,
angamve ndi makutu ao, angazindikire ndi mtima wao,
nakabwerenso, naciritsidwe. 11Pompo ndinati ine, Ambuye mpaka
liti? Ndipo anayankha, Mpaka midzi ikhala bwinja, yopanda
wokhalamo, ndi nyumba zopanda munthu, ndi dziko likhala bwinja
ndithu, 12ndipo Yehova wasunthira anthu kutari, ndi mabwinja
adzacuruka pakati pa dziko. 13Ndipo likatsala limodzi la magawo
khumi m'menemo, lidzadyedwanso; monga kacere, ndi monganso
thundu, imene tsinde lace likhalabe ataigwetsa; cotero mbeu
yopatulika ndiyo tsinde lace.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Rezini ndi Peka akwerera Yerusalemu

1Ndipo panali masiku a Ahazi, mwana wa Yotamu, mwana wa
Uziya, mfumu ya Yuda, kuti Rezini, mfumu ya Aramu, ndi Peka,
mwana wa Remaliya, mfumu ya Israyeli, anakwera kunka ku
Yerusalemu, kumenyana nao; koma sanathe kuupamnana. 2Ndipo
anauza a nyumba ya Davide, kuti Aramu wapangana ndi Efraimu.
Ndipo mtima wace unagwedezeka, ndi mtima wa anthu ace,
monga mitengo ya m'nkhalango igwedezeka ndi mphepo. 3Ndipo
Yehova anati kwa Yesaya, Turuka tsopano kukacingamira Ahazi, iwe
ndi Seariyasubu, mwana wamwamuna wako, pa mamariziro a
mcerenje wa thamanda la pamtunda, ku khwalala la pa mwaniko
wa wotsuka nsaru; 4nukati kwa iye, Cenjera, khala ulipo; usaope,
mtima wako usalefuke, cifukwa ca zidutswa ziwirizi za miuni
yofuka, cifukwa ca mkwiyo waukali wa Rezini ndi Aramu, ndi wa
mwana wa Remaliya. 5Cifukwa Aramu ndi Efraimu, ndi mwana wa
Remaliya anapangana kukucitira zoipa, nati, 6Tiyeni, tikwere,
timenyane ndi Yuda, timbvute; tiyeni, tidzigumulire mpata,
pamenepo tikhazike mfumu pakati pace, ngakhale mwana
wamwamuna wa Tabeeli; 7atero Ambuye Yehova, Upo wao
sudzaimai, sudzacitidwa. 8Pakuti mutu wa Aramu ndi Damasiko,
ndi mutu wa Damasiko ndi Rezini, zisadapite zaka makumi asanu
ndi limodzi mphambu zisanu Efraimu adzatyokatyoka,
sadzakhalanso mtundu wa anthu; 9ndipo mutu wa Efraimu ndi
Samariya, ndi mutu wa Samariya ndi mwana wa Remaliya,
mukapanda kukhulupirira ndithu simudzakhazikika.

Lonjezo lakunena za Imanueli

10Ndipo Yehova ananenanso kwa Ahazi nati, 11Udzipemphere
wekha cizindikilo ca kwa Yehova Mulungu wako; pempha
cam'mwakuya, kapena cam'mwamba. 12Koma Ahazi anati,
Sindipemphai ngakhale kumyesa Yehova. 13Ndipo iye anati,
Mverani inu tsopano, inu a nyumba ya Davide; kodi ndi kanthu
kakang'ono kwa inu kutopetsa anthu, kuti inu mutopetsa Mulungu
wanga? 14Cifukwa cace Ambuye mwini yekha adzakupatsani inu
cizindikilo; taonani namwali adzaima, nadzabala mwana
wamwamuna, nadzamucha dzina lace Imanueli. 15Iye adzadya
mafuta ndi uci, pamene adziwa kukana coipa ndi kusankha
cabwino. 16Popeza kuti asanadziwe mwanayo kukana coipa ndi
kusankha cabwino, dziko limene mafumu ace awiri udana nao
lidzasyidwa. 17Yehova adzatengera pa iwe, ndi pa anthu ako, ndi
pa nyumba ya atate wako, masiku, akuti sanadze oterewa
kuyambira tsiku limene Efraimu analekana ndi Yuda; kunena
mfumu ya Asuri.

18Ndipo padzakhala tsiku limenelo kuti Yehova adzayimbira mluzu
cimphanga ciri m'mbali ya kumtunda kwa nyanja za Aigupto, ndi
njuci iri m'dziko la Asuri. 19Ndipo zidzafika nizitera zonse m'zigwa
zabwinja, ndi m'maenje a matanthwe, ndi paminga ponse, ndi
pamabusa ponse.
20Tsiku limenelo Ambuye adzameta mutu, ndi ubweya wa
m'mapazi, ndi lumo lobwereka liri tsidya lija la Nyanja, kunena
mfumu ya Asuri; ndilo lidzamarizanso ndebvu.
21Ndipo padzakhala tsiku limenelo, kuti munthu adzaweta ng'ombe
yaikazi yaing'ono, ndi nkhosa ziwiri; 22ndipo padzakhala, cifukwa
ca kucuruka kwa mkaka umene zidzapatsa, iye adzadya mafuta;
pakuti mafuta ndi uci adzadya yense wosiyidwa pakati pa dziko.
23Ndipo padzakhala tsiku limenelo, kuti pali ponse panali mipesa
cikwi cimodzi ya mtengo wace wa ndalama cikwi cimodzi,
padzakhala lunguzi ndi minga. 24Munthu adzafikako ndi mibvi ndi
uta; pakuti dziko lonse lidzakhala la lunguzi ndi minga. 25Ndipo
zitunda zonse zinalimidwa ndi khasu, iwe sudzafikako cifukwa ca
kuopa lunguzi ndi minga, koma pomwepo padzakhala potumizira
ng'ombe ndi popondaponda nkhosa.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Coneneratu cakuti Aasuri adzagonjetsa Israyeli

1Ndipo Yehova anati kwa ine, Tenga iwe polembapo papakuru,
nulembe pamenepo ndi malembedwe odziwika, Kangazakufunkha
Fulumirakusakaza, 2Ndipo ndidzadzitengera ine mboni
zokhulupirika, Uriya wansembe, ndi Zekariya mwana wa
Yeberekiya. 3Ndipo ndinanka kwa mneneri wamkazi; ndipo iye
anatenga pakati nabala mwana wamwamuna. Ndipo Yehova anati
kwa ine, Uche dzina lace, Kangazakufunkha
Fulumirakusakaza. 4Cifukwa kuti mwana asakhale ndi nzeru
yakupfuula, Atate wanga, ndi Amai wanga, cuma ca Damasiko ndi
cofunkha ca Samariya cidzalandidwa pamaso pa mfumu ya Asuri.
5Ndipo Yehova ananena kwa ine kaciwirinso, nati, 6Popeza anthu
awa akana madzi a Silowa, amene ayenda pang'ono pang'ono,
nakondwerera mwa Rezini ndi mwa mwana wa Remaliya; 7cifukwa
cace, taonani, Ambuye atengera pa iwo madzi a Nyanja, olimba
ndi ambiri, kunena mfumu ya Asuri ndi ulemerero wace wonse;
ndipo iye adzadzala mphaluka zace zonse, nadzasefukira
pamtunda ponse. 8Ndipo iye adzapitapitakulowa m'Yuda;
adzasefukira, napitirira; adzafikira m'khosi; ndi kutambasula kwa
mapiko ace, kudzakwanira dziko lanu m'citando mwace, inu
Imanueli.
9Citani phokoso, anthu inu, koma mudzatyokatyoka; cherani khutu,
inu nonse a maiko akutari; kwindani nokha, koma
mudzatyokatyoka; kwindani nokha, koma
mudzatyokatyoka. 10Panganani upo, koma udzakhala cabe; nenani
mau, koma sadzacitika; pakuti Mulungu ali pamodzi ndi
ife. 11Pakuti Yehova watero kwa ine ndi dzanja lolimba,
nandilangiza ine kuti ndisayende m'njira ya anthu awa,
nati, 12Musacinene, Ciwembu; ciri conse cimene anthu awa
adzacinena, Ciwembu; musaope monga kuopa kwao kapena
musacite mantha. 13Yehova wa makamu, Iye mudzamyeretsa;
muope Iye, akucititseni mantha Iye. 14Ndipo Iye adzakhala malo
opatulika; koma mwala wopunthwitsa, ndi thanthwe lolakwitsa la
nyumba zonse ziwiri za Israyeli, khwekhwe ndi msampha wa
okhala m'Yerusalemu. 15Ndipo ambiri adzapunthwapo, nagwa,
natyoka, nakodwa, natengedwa.
16Manga umboni, mata cizindikilo pacilamulo mwa aphunzi
anga. 17Ndipo ndidzalindira Yehova, amene wabisira a nyumba ya
Yakobo nkhope yace, ndipo ndidzamyembekeza Iye, 18Taonani, ine
ndi ana amene Yehova wandipatsa ine, tiri zizindikilo ndi
zodabwitsa mwa Israyeli, kucokera kwa Yehova wa makamu,
amene akhala m'phiri la Ziyoni.

19Ndipo pamene iwo adzati kwa iwe, Funa kwa olaula, ndi
obwebweta, amene alira pyepye, nang'ung'udza; kodi anthu
sadzafuna kwa Mulungu wao? Cifukwa ca amoyo, kodi adzafuna
kwa akufa? 20Kucilamulo ndi kuumboni! ngati iwo sanena malinga
ndi mau awa, ndithu sadzaona mbanda kuca. 21Ndipo iwo
adzapitirira obvutidwa ndi anjala, ndipo padzakhala kuti pokhala
ndi njala iwo adzadziputa okha, ndi kutemberera mfumu yao, ndi
Mulungu wao; ndi kugadamira nkhope zao
kumwamba; 22nadzayang'ana padziko, koma taonani, nkhawa ndi
mdima, kuziya kwa nsautso; ndi mdima woti bi udzaingitsidwa.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Coneneratu ca ufumu wa Mesiya

1Koma kumene kunali nsautso sikudzakhala kuziya. Poyamba paja
Mulungu ananyozetsa dziko la Zebuloni, ndi dziko la Naftali, koma
potsiriza pace Iye analicitira ulemu, pa khwalala la kunyanja,
patsidya pa Yordano, Galileya wa amitundu. 2Anthu amene
anayenda mumdima, aona kuwala kwakukuru; iwo amene
anakhala m'dziko la mthunzi wa imfa, kuwala kwaturukira kwa
iwo. 3Inu mwacurukitsa mtundu, inu mwaenjezera kukondwa kwao;
iwo akondwa pamaso panu monga akondwera m'masika, monga
anthu akondwa pogawana zofunkha. 4Pakuti gori la katundu wace,
ndi mkunkhu wa paphewa pace, ndodo ya womsautsa, inu
mwazityola monga tsiku la Midyani. 5Pakuti zida zonse za
mwamuna wobvala zida za nkhondo m'phokosomo, ndi zobvala
zobvimvinika m'mwazi, zidzakhala zonyeka ngati nkhuni. 6Pakuti
kwa ife mwana wakhanda wabadwa, kwa ife mwana wamwamuna
wapatsidwa; ndipo ulamuliro udzakhala pa phewa lace, ndipo
adzamucha dzina lace Wodabwitsa, Wauphungu, Mulungu
wamphamvu, Atate Wosatha, Kalonga wa mtendere. 7Za
kuenjezera ulamuliro wace, ndi za mtendere sizidzatha pa mpando
wacifumu wa Davide, ndi pa ufumu wace, kuukhazikirsa, ndi
kuucirikiza ndi ciweruziro ndi cilungamo kuyambira tsopano ndi
kunkabe nthawi zonse. Cangu ca Yehova wa makamu cidzacita
zimenezi.

Aisrayeli Acenjezedwa kuti adzalangidwa

8Ambuye anatumiza mau kwa Yakobo, ndipo anatsikira pa
Israyeli. 9Ndipo anthu onse adzadziwa, ngakhale Efraimu ndi
okhala m'Samariya, amene anena m'kunyada ndi m'kukula kwa
mtima, 10Njerwa zagwa, koma ife tidzamanga ndi miyala yosema;
mikuyu yagwetsedwa, koma tidzaisinthanitsa ndi
mikungudza. 11Cifukwa cace Yehova adzamkwezera Rezini
olimbana naye, nautsa adani ace; 12Aramu patsogolo ndi Afilisti
pambuyo; ndipo iwo adzadya Israyeli ndi kukamwa koyasama.
Mwa izi zonse mkwiyo wace sunacoke, koma dzanja lace liri
citambasulire.
13Koma anthu sanatembenukire kwa Iye amene anawamenya,
ngakhale kufuna Yehova wa makamu. 14Cifukwa cace Yehova
adzadula mutu wa Israyeli ndi mcira wace; nthambi ya kanjedza
ndi mlulu, tsiku limodzi. 15Nkhalamba ndi wolemekezeka ndiye
mutu, ndi mneneri wophunzitsa zonama ndiye mcira. 16Pakuti iwo
amene atsogolera anthuwa, ndiwo awasokeretsa; ndipo iwo amene
atsogoleredwa nao aonongeka. 17Cifukwa cace Ambuye
sadzakondwera ndi anyamata ao, ngakhale kuwacitira cifundo
amasiye ao ana ndi akazi; popeza yense ali wodetsa ndi wocimwa,

m'kamwa monse mulankhula zopusa. Mwa izi zonse mkwiyo wace
sunacoke, koma dzanja lace liri citambasulire.
18Pakuti kucimwa kwayaka ngati moto kumariza lunguzi ndi minga,
inde kuyaka m'nkhalango ya m'thengo, ndipo zifuka capamwamba,
m'mitambo yautsi yocindikira. 19M'kukwiya kwa Yehova wa
makamu, dziko latenthedwa ndithu, anthunso ali ngati nkhuni;
palibe munthu wocitira mbale wace cisoni. 20Ndipo wina
adzakwatula ndi dzanja lamanja, nakhala ndi njala; ndipo adzadya
ndi dzanja lamanzere, osakhutai; iwo adzadya munthu yense
nyama ya mkono wace wa iye mwini. 21Manase adzadya Efraimu
ndi Efraimu adzadya Manase, ndipo iwo pamodzi adzadyana ndi
Yuda. Mwa izi zonse mkwiyo wace sunacoke, koma dzanja lace liri
citambasulire.

©The Bible Society of Malawi, 1992

1Tsoka kwa iwo amene alamulira malamulo osalungama, ndi kwa
alembi olemba mphulupulu; 2kuwapatulira osowa kuciweruziro, ndi
kucotsera anthu anga aumphawi zoyenera zao, kuti alande za akazi
amasiye, nafunkhire ana amasiye! 3Ndipo mudzacita ciani tsiku
lakudza woyang'anira, ndi cipasuko cocokera kutari? mudzathawira
kwa yani kufuna kuthangatidwa? mudzasiya kuti ulemerero
wanu? 4Adzangoweramira pansi pa andende, ndipo adzagwa pansi
pa ophedwa. Mwa izi zonse mkwiyo wace sunacoke, koma dzanja
lace liri citambasulire.

Aneneratu za kuonongeka kwa kuti

5Iwe Asuri cibonga ca mkwiyo wanga, ndodo m'dzanja lace muli
ukali wanga! 6Ine ndidzamtumiza kumenyana ndi mtundu
wosalemekeza, ndi pa anthu a mkwiyo wanga ndidzamlangiza, kuti
afunkhe, agwire zolanda, awapondereze pansi, monga dothi la
pamakwalala. 7Koma iye safuna cotero, ndipo mtima wace
suganizira cotero, koma mtima wace ulikufuna kusakaza, ndi
kuduladula amitundu osawerengeka. 8Popeza ati, Akalonga anga
kodi sali onse mafumu? 9Kodi Kalino sali wonga ngati Karikemesi?
kodi Hamati sali ngati Aripadi? kodi Samariya sali ngati
Damasiko? 10Popeza dzanja langa lapeza maufumu a mafano,
mafano ao osema anapambana ndi iwo a ku Yerusalemu ndi ku
Samariya; 11monga ndacitira Samariya ndi mafano ace, momwemo
kodi sindidzacitira Yerusalemu ndi mafano ace?
12Cifukwa cace padzaoneka, kuti pamene Ambuye atatha nchito
yace yonse pa phiri la Ziyoni ndi pa Yerusalemu, ndidzalanga
zipatso za mtima wolimba wa mfumu ya Asuri, ndi ulemerero wa
maso ace okwezedwa. 13Popeza anati, Mwa mphamvu ya dzanja
langa ndacita ici, ndi mwa nzeru yanga; pakuti ine ndiri wocenjera;
ndacotsa malekezero a anthu, ndalanda cuma cao, ndagwetsa
monga munthu wolimba mtima iwo okhala pa mipando
yacifumu; 14dzanja langa lapeza monga cisa, cuma ca mitundu ya
anthu, ndipo monga munthu asonkhanitsa mazira osiyidwa, ine
ndasonkhanitsa dziko lonse lapansi, ndipo panalibe cogwedeza
phiko, kapena cotsegula pakamwa, kapena colira pyepye. 15Kodi
nkhwangwa idzadzikweza yokha, pa iye amene adula nayo? kodi
cocekera cidzadzikweza cokha pa iye amene acigwedeza, ngati
cibonga ingamgwedeze iye amene ainyamula, ngati ndodo
inganyamule kanthu popeza iri mtengo.
16Cifukwa cace Ambuye, Yehova wa makamu, adzarumiza kuonda
mwa onenepa ace; ndipo pansi pa ulemerero wace padzayaka
kutentha, konga ngati kutentha kwa moto. 17Ndipo kuwala kwa
Israyeli kudzakhala moto, ndi Woyera wace adzakhala lawi; ndipo
lidzatentha ndi kuthetsa minga yace ndi lunguzi wace tsiku

limodzi. 18Ndipo adzanyeketsa ulemerero wa m'nkhalango yace,
ndi wa m'munda wace wopatsa bwino, moyo ndi thupi; ndipo
padzakhala monga ngati pokomoka wonyamula
mbendera. 19Ndipo mitengo yotsala ya m'nkhalango yace
idzakhala yowerengeka, kuti mwana ailembera.
20Ndipo padzakhala tsiku lomwelo, kuti otsala a Israyeli, ndi iwo
amene anapulumuka a nyumba ya Yakobo, sadzatsamiranso iye
amene anawamenya; koma adzatsamira Yehova Woyera wa
Israyeli, ntheradi. 21Otsala adzabwera, otsala a Yakobo, kwa
Mulungu wamphamvu. 22Popeza ngakhale anthu anu Israyeli
akunga mcenga wa kunyanja, otsala ao okha okha adzabwera;
cionongeko catsimikizidwa, cilungamo cace cisefukira. 23Pakuti
Ambuye Yehova wa makamu adzacita cionongeko cotsimikizidwa
pakati pa dziko lonse lapansi.
24Cifukwa cace atero Ambuye; Yehova wa makamu, Inu anthu anga
okhala m'Ziyoni, musaope Asuri; ngakhale amenya inu ndi
cibonga, kapena kukusamulira iwe ndodo yace, monga amacitira
Aigupto. 25Pakuti patsala kamphindi, ndipo ukali udzathedwa ndi
mkwiyo wanga wakuwaononga. 26Ndipo Yehova wa makamu
adzamuutsira cikoti, monga m'kuphedwa kwa Midyani pa thanthwe
la Orebu; ndipo cibonga cace cidzakhala pamwamba pa nyanja,
ndipo adzaisamula monga anacitira Aigupto, 27Ndipo padzakhala
tsiku lomwelo, kuti katundu wace adzacoka pa phewa lako, ndi gori
lace pakhosi pako; ndipo gori lidzathedwa cifukwa ca kudzoza
mafuta.
28Wafika ku Aiati, wapitirira kunka ku Migroni; pa Mikimasi asunga
akatundu ace; 29wapita pampata; wagona pa Geba, Rama
anthunthumira; Gibeya wa Sauli wathawa. 30Pfuula ndi mau ako
iwe mwana wamkazi wa Galimu! tamva, iwe Laisa! iwe Anatoti
wosauka! 31Madimena ali wothawathawa; okhala m'Gebimu
asonkhanakutiathawe. 32Lero lomwe adzaima pa Nobu;
agwedezera dzanja lace pa phiri la mwana wamkazi wa Ziyoni,
phiri la Yerusalemu.
33Taonani, Ambuye Yehova wa makamu adzasadza nthambi
moopsya; ndipo zazitari msinkhu zidzadulidwa, ndipo zazitari
zidzagwetsedwa. 34Ndipo adzadula nkhalango za m'thengo ndi
citsulo, ndipo Lebano adzagwa ndi wamphamvu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Ufumu wa mtendere wa Mesiya

1Ndipo padzaturuka mphukira pa tsinde la Jese, ndi nthambi
yoturuka m'mizu yace idzabala zipatso; 2ndipo mzimu wa Yehova
udzambalira iye mzimu wanzeru ndi wakuzindikira, mzimu wa
uphungu ndi mphamvu, mzimu wakudziwa ndi wakuopa
Yehova; 3ndipo adzakondwera nako kumuopa Yehova, ndipo
sadzaweruza monga apenya maso, sadzadzudzula
mwamphekesera: 4koma ndi cilungamo adzaweruza aumphawi,
nadzadzudzulira ofatsa a m'dziko moongoka; ndipo adzamenya
dziko lapansi ndi cibonga ca kukamwa kwace, nadzapha oipa ndi
mpweya wa milomo yace. 5Ndipo cilungamo cidzakhala mpango
wa m'cuuno mwace, ndi cikhulupiriko cidzakhala mpango wa pa
zimpsyo zace. 6Mmbulu udzakhala pamodzi ndi mwana wa nkhosa,
ndipo nyalugwe adzagona pansi ndi mwana wa mbuzi; ndipo
mwana wa ng'ombe ndi mwana wa mkango ndi coweta conenepa
pamodzi; ndipo mwana wamng'ono adzazitsogolera. 7Ndipo
ng'ombe yaikazi ndi cirombo zidzadya pamodzi; ndipo ana ao
ang'ono adzagona pansi; ndipo mkango udzadya udzu ngati
ng'ombe. 8Ndipo mwana wakuyamwa adzasewera pa una wa
mamba, ndi mwana woleka kuyamwa adzaika dzanja lace
m'pfunkha la mphiri. 9Sizidzaipitsa, sizidzasakaza m'phiri langa
lonse loyera, cifukwa kuti dziko lapansi lidzadzala ndi odziwa
Yehova, monga mdazi adzaza nyanja.
10Ndipo padzakhala tsiku lomwelo, kuti muzu wa Jese umene uima
ngati mbendera ya mitundu ya anthu, amitundu adzafunafuna
uwu; ndipo popuma pace padzakhala ulemerero.
11Ndipo padzakhala tsiku lomwelo, kuti Ambuye adzabweza
kaciwiri ndi dzanja lace anthu ace otsala ocokera ku Asuri, ndi ku
Aigupto, ndi ku Patirosi, ndi ku Kusi, ndi ku Elamu, ndi ku Sinara,
ndi ku Hamati, ndi ku zisumbu za m'nyanja yamcere. 12Ndipo Iye
adzaimika mbendera ya amitundu, ndipo adzasonkhanitsa
oingitsidwa a Israyeli, namema obalalika a Yuda, kucokera ku
madera anai a dziko lapansi. 13Ndipo nsanje ya Efraimu idzacoka,
ndi iwo amene abvuta Yuda adzadulidwa; Efraimu sacitira nsanje
Yuda, ndi Yuda sacitira nsanje Efraimu. 14Ndipo adzagudukira
mapewa a Afilisti kumadzulo; pamodzi adzafunkha ana a
kum'mawa; adzatambasula dzanja lao pa Edomu ndi pa Moabu;
ndipo ana a Amoni adzawamvera. 15Ndipo Yehova adzaononga
ndithu bondo la nyanja ya Aigupto; ndipo ndi mphepo yace
yopsereza adzagwedeza dzanja lace pa Nyanja, ndipo adzaimenya
ikhale mphaluka zisanu ndi ziwiri, nadzaolotsa anthu pansi
pouma. 16Ndipo padzakhala khwalala la anthu ace otsala ocokera

ku Asuri; monga lija la Israyeli tsiku lokwera iwo kuturuka m'dziko la Aigupto.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Ciyamiko ca anthu a Mulungu atalangidwa

1Tsiku lomwelo udzati, Ndikuyamikani inu Yehova; pakuti ngakhale
munandikwiyira, mkwiyo wanu wacoka, ndipo mutonthoza mtima
wanga. 2Taonani, Mulungu ndiye cipulumutso canga;
ndidzakhulupira, sindidzaopa; pakuti Yehova Mwini ndiye mphamvu
yanga ndi nyimbo yanga, Iye ndiye cipulumutso canga. 3Cifukwa
cace mudzakondwera pakutunga madzi m'zitsime za
cipulumutso. 4Tsiku lomwelo mudzati, Muyamikire Yehova,
bukitsani dzina lace, mulalikire macitidwe ace mwa mitundu ya
anthu, munene kuti dzina lace lakwezedwa. 5Muyimbire Yehova;
pakuti wacita zaulemerero; cidziwike ici m'dziko lonse. 6Tapfuula,
takuwa iwe, wokhala m'Ziyoni, cifukwa Woyera wa Israyeli wa
m'kati mwako ali wamkuru.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Aneneratu za kutyoka kwa ufumu wa Babulo, ndi kubweza Israyeli kwao

1Katundu wa Babulo, imene anaiona Yesaya mwana wa Amozi.
2Kwezani mbendera pa phiri loti se, kwezani mau kwa iwo,
kodolani kuti alowe m'zipata za akuru. 3Ine ndalamulira opatulidwa
anga, inde, ndaitana amphamvu anga, acite mkwiyo wanga,
okondwerera ndi ukuru wanga. 4Mau a khamu m'mapiri, akunga
amtundu waukuru wa anthu, mau a phokoso la maufumu a
mitundu yosonkhanidwa! Yehova wa makamu asonkhanitsa khamu
kunkhondo. 5Acokera m'dziko lakutari, ku malekezero a thambo,
ngakhale Yehova, ndi zida za mkwiyo wace, kuti aononge dziko
lonse. 6Kuwani inu; pakuti tsiku la Yehova liri pafupi; lidzafika
monga cionongeko cocokera kwa Wamphamvuyonse. 7Cifukwa
cace manja onse adzafoka, ndi mitima yonse ya anthu
idzasungunuka; 8ndipo adzaopa; zowawa ndi masauko
zidzawagwira; ndipo adzamva zowawa, ngati mkazi wakubala;
adzazizwa wina ndi wina; nkhope zao zidzanga malawi a
moto. 9Taonani tsiku la Yehova lidza, lankhanza, ndi mkwiyo ndi
kukalipira kwaukali; kupasula dziko, ndi kudzaonongamo akucimwa
psiti. 10Cifukwa nyenyezi za kumwamba ndi makamu ao
sizidzawala; dzuwa lidzada m'kuturuka kwace, ndipo mwezi
sudzaonetsa kuwala kwace. 11Ndipo ndidzalanga dziko lapansi,
cifukwa ca kuipa kwao, ndi oipa cifukwa ca mphulupulu zao; ndipo
ndidzaletsa kudzikuza kwa onyada, ndidzagwetsa kudzikweza kwa
oopsya. 12Ndipo ndidzacepsa anthu koposa golidi, ngakhale anthu
koposa golidi weniweni wa ku Ofiri. 13Cifukwa cace
ndidzanthunthumiritsa miyamba, ndipo dziko lapansi
lidzagwedezeka kucokera m'malo ace, m'mkwiyo wa Yehova wa
makamu, tsiku la mkwiyo wace waukali. 14Ndipo padzakhala kuti
monga mbawala yothamangitsidwa, ndi monga nkhosa
zosazisonkhanitsa anthu, adzatembenukira yense kwa anthu ace,
nathawira yense ku dziko lace. 15Onse opezedwa adzapyozedwa,
ndi onse ogwidwa adzagwa ndi lupanga. 16Makanda ao
adzatswanyidwe pamaso pao; m'nyumba mwao mudzafunkhidwa,
ndi akazi ao adzakakamizidwa. 17Taonani, ndidzawautsira Amedi,
amene sadzasamalira siliva, ngakhale golidi sadzakondwera
naye. 18Mauta ao adzatha anyamata; ndipo sadzacitira cisoni
cipatso ca mimba; diso lao silidzaleka ana. 19Ndipo Babulo,
ulemerero wa maufumu, mudzi wokongolawo Akasidi anaunyadira,
adzakhala monga momwe Mulungu anapasula Sodomu ndi
Gomora. 20Anthu sadzakhalamo konse, sadzakhalamo mbadwo ndi
mbadwo; M-arabu sadzamanga hema wace pamenepo; abusa
sadzagonetsa makamu ao kumeneko. 21Koma zirombo za

m'cipululu zidzagona pamenepo; nyumba zao zidzadzala ndi zakukuwa; ndipo nthiwatiwa zidzakhala pamenepo, ndipo atonde adzajidimuka pamenepo, 22Ndipo mimbulu idzalira m'maboma ao, ndi ankhandwe m'manyumba ao abwino; ndi nthawi yace iyandikira, ndi masiku ace sadzacuruka.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Yesaya 14

1Pakuti Ambuye adzamcitira cifundo Yakobo, ndipo adzasankhanso
Israyeli, ndi kuwakhazikitsa m'dziko la kwao; ndipo acilendo
adzadziphatika okha kwa iwo, nadzadzigumikiza ku nyumba ya
Yakobo. 2Ndipo mitundu ya anthu idzawatenga, ndi kuwafikitsa ku
malo a kwao; ndipo a nyumba ya Israyeli adzakhala nao
amitunduwo m'dziko la Yehova, ndi kuwayesa atumiki ndi adzakazi,
ndipo amitunduwo adzatengedwa ndende, ndi amenewo anali
ndende zao; ndipo Aisrayeli adzalamulira owabvuta.
3Ndipo padzakhala tsiku loti Yehova adzakupumitsa cisoni cako, ndi
nsautso yako, ndi nchito yako yobvuta, imene
anakugwiritsa, 4pamenepo udzayimbira mfumu ya ku Babulo
nyimbo iyi yancinci, ndi kuti, Wobvuta wathadi! mudzi wagolidi
wathadi! 5Yehova watyola mkunkhu wa woipa, ndodo yacifumu ya
wolamulira. 6Wokantha anthu mwaukali kuwakantha cikanthire,
wolamulira amitundu mokwiya, angosautsidwa wopanda
womlanditsa. 7Dziko lonse lapuma, liri du; iwo ayamba kuyimba
nyimbo, 8Inde, milombwa ikondwera ndi iwe, ndi mikungudza ya
Lebano, ndi kunena, Cigwetsere iwe pansi, palibe wokwera
kudzatidula ife. 9Kunsi kwa manda kugwedezeka, cifukwa ca iwe,
kukucingamira podza pako; kukuutsira iwe mizimu, ngakhale onse
akuru akuru a dziko lapansi; kukweza kucokera m'mipando yao
mafumu onse a amitundu. 10Onse adzabvomera, nadzati kwa iwe,
Kodi iwe wakhalanso wopanda mphamvu ngati ife? kodi iwe
wafanana nafe? 11Cifumu cako catsitsidwa kunsi ku manda, ndi
phokoso la mingoli yako; mbozi zayalidwa pansi pa iwe, ndi
mphukutu zakukuta. 12Wagwadi kucokera kumwamba, iwe
nthanda, mwana wa mbanda kuca! Wagwetsedwa pansi, iwe
wolefula amitundu! 13Ndipo iwe unati mumtima mwako,
Ndidzakwera kumwamba, ndidzakweza mpando wanga wacifumu
pamwamba pa nyenyezi za Mulungu; ndidzakhala pamwamba pa
phiri la khamu, m'malekezero a kumpoto; 14ndidzakwera
pamwamba pa mitambo, ndidzafanana ndi
Wam'mwambamwamba. 15Koma udzatsitsidwa kunsi ku manda, ku
malekezero a dzenje. 16Iwo amene akuona iwe adzayang'anitsitsa
iwe, nadzalingalira za iwe, ndi kuti, Kodi uyu ndi munthu amene
ananthunthumiritsa dziko lapansi, amene anagwedeza
maufumu; 17amene anapululutsa dziko, napasula midzi yace,
amene sanamasula ndende zace, zinke kwao? 18Mafumu onse a
amitundu, onsewo agona m'ulemerero yense kunyumba
kwace. 19Koma iwe watayidwa kunja kwa manda ako, ngati
nthambi yonyansa, ngati cobvala ca ophedwa, opyozedwa ndi
lupanga, otsikira ku miyala ya dzenje, monga ngati mtembo
wopondedwa ndi phazi. 20Iwe sudzaphatikizidwa pamodzi nao

poikidwa, pakuti iwe waononga dziko lako, wapha anthu ako; mbeu
ya ocita zoipa sidzachulidwa konse. 21Konzani inu popherapo ana
ace, cifukwa ca kuipa kwa atate ao; kuti iwo asadzauka ndi kukhala
nalo dziko, ndi kudzaza dziko lapansi ndi midzi. 22Ndipo Ine
ndidzawaukira, ati Yehova wa makamu, ndi kuononga ku Babulo
dzina ndi otsala, ndi mwana wamwamuna, ndi cidzukulu cacimuna,
ati Yehova. 23Ndidzayesapo pokhala nungu, ndi madziwe a madzi;
ndipo ndidzasesapo ndi tsace la cionongeko, ati Yehova wa
makamu.

Aneneratu za kutyoka kwa Asuri

24Yehova wa makamu walumbira, nati, Ndithu monga ndaganiza,
cotero cidzacitidwa; ndipo monga ndapanga uphungu, cotero
cidzakhala; 25kuti Ine ndidzatyola Asuri m'dziko langa, ndi
pamwamba pa mapiri anga ndidzawapondereza; pomwepo gori
lace lidzacoka pa iwo, ndi katundu wace adzacoka paphuzi
pao. 26Umenewu ndi uphungu wopangira dziko lonse; ndipo ili ndi
dzanja lotambasulidwa pa amitundu onse. 27Pakuti Yehova wa
makamu wapanga uphungu, ndani adzauleketsa? ndi dzanja lace
latambasulidwa, ndani adzalibweza?

Aneneratu za tsoka la Afilisti

28Caka cimene mfumu Ahazi anamwalira katundu amene analipo.
29Usakondwere, lwe Filistia, wonsewe, potyoka ndodo inakumenya;
pakuti m'muzu wa njoka mudzaturuka mphiri, ndimo cipatso cace
cidzakhala njoka yamoto youluka. 30Ndi oyamba kubadwa a
osauka adzadya, aumphawi nadzagona pansi osatekeseka; ndipo
ndidzapha muzu wako ndi njala, ndi otsala ako adzaphedwa. 31Lira,
cipata iwe; pfuula, mudzi iwe; wasungunuka, Filistia wonsewe,
pakuti utsi ucokera kumpoto, ndipo palibe wosokera m'mizere
yace. 32Ndipo adzayankhanji amithenga a amitundu? Kuti Yehova
wakhazikitsa Ziyoni, ndipo m'menemo anthu ace obvutidwa
adzaona pobisalira.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Aneneratu za kuonongeka kwa Moabu

1Katundu wa Moabu.
Pakuti usiku umodzi Ara wa ku Moabu wapasuka, nakhala cabe;
usiku umodzi Kiri wa Moabu wapasuka, nakhala cabe. 2Akwera
kukacisi, ndi ku Dibo, kumisanje, kukalira; pa Nebo ndi pa Medeba
a Moabu pali kulira; pamitu pao ponse pali dazi, ndebvu zonse
zametedwa. 3M'makwalala mwao adzimangira ciguduli m'cuuno,
pamwamba pa nyumba zao, ndi m'malo a mabwalo ao, yense
akuwa, naliritsa kwambiri. 4Ndi Hesiboni apfuula zolimba, ndi
Eliale; mau ao amveka, ngakhale ku Yahazi; cifukwa cace amuna
ankhondo a Moabu apfuula zolimba; moyo wace wanthunthumira
m'kati mwace. 5Mtima wanga upfuula cifukwa ca Moabu: akuru ace
athawira ku Zoari, ku Eglatiselisiya; pakuti pa cikweza ca Luhiti
akwera alikulira, pakuti m'njira ya Horanaimu akweza mpfuu wa
cionongeko. 6Pakuti pa madzi a Nimirimi padzakhala mabwinja;
papeza udzu wafota, msipu watha. 7Cifukwa cace zocuruka
adazipeza, ndi zosungidwa zao adzazitenga kunka nazo ku mtsinje
wa mabango. 8Pakuti kulira kwamveka kuzungulira malire a
Moabu; kukuwa kwace kwafikira ku Eglaimu, ndi kukuwa kwace
kwafikira ku Beerelimu. 9Pakuti madzi a Dimoni adzala mwazi;
pakuti ndidzatengera zina pa! Dimoni, mkango pa iye amene
anapulumuka ku Moabu, ndi pa otsala am'dziko.

©The Bible Society of Malawi, 1992

1Tumizani inu ana a nkhosa kwa wolamulira wa dziko kucokera ku
Sela kunka kucipululu, mpaka ku phiri la mwana wamkazi wa
Ziyoni. 2Pakuti ana akazi a Moabu adzakhala pa madooko a Arinoni,
ngati mbalame zoyendayenda, ngati cisa cofwancuka. 3Citani
uphungu, weruzani ciweruziro; yesa mthunzi wako monga usiku
pakati pa usana; bisa opitikitsidwa, osaulula
woyendayenda. 4Opitikitsidwa a Moabu akhale ndi iwe, khala iwe
comphimba pamaso pa wofunkha; pakuti kumpambapamba
kwalekeka, kufunkha kwatha, opondereza atsirizika m'dziko. 5Ndipo
mpando wacifumu udzakhazikika m'cifundo, ndimo wina adzakhala
pamenepo m'zoona, m'cihema ca Davide, nadzaweruza,
nadzafunitsa ciweruziro, nadzafulumira kucita cilungamo.
6Ife tinamva kunyada kwa Moabu, kuti iye ali wonyada ndithu;
ngakhale kudzitama kwace, ndi kunyada kwace ndi mkwiyo wace;
matukutuku ace ali acabe. 7Cifukwa cace Moabu adzakuwa cifukwa
ca Moabu, onse adzakuwa; cifukwa ca maziko a Kirihareseti
mudzalira maliro, osautsidwa ndithu. 8Pakuti minda ya ku Hesiboni
yalefuka, ndi mpesa wa ku Sibimai; ambuye a mitundu atyolatyola
mitengo yosankhika yace; iwo anafikira ngakhale ku Yazeri,
nayendayenda m'cipululu; nthambi zace zinatasa, zinapitima
panyanja. 9Cifukwa cace ndidzalira ndi kulira kwa Yazeri, cifukwa
ca mpesa wa Sibima, ndidzakukhathamiza ndi misozi yanga, iwe
Hesiboni ndi Eleale; cifukwa kuti pa zipatso zako za malimwe, ndi
pa masika ako, mpfuu wankhondo wagwera. 10Ndipo cikondwero
ndi msangalalo zacotsedwa m'munda wapatsa zipatso; ndi
m'minda ya mipesa simudzakhala kuyimba, ngakhale phokoso
losangalala; palibe woponda adzaponda vinyo m'moponderamo;
ndaleketsa mpfuu wa masika amphesa. 11Cifukwa cace m'mimba
mwanga mulirira Moabu, ngati mngoli, ndi za m'mtima mwanga
zilirira Kiriheresi. 12Ndipo padzakhala kuti pamene Moabu
adzadzionetsa yekha, ndi kudzitopetsa pamsanje, ndipo kufika ku
malo ace oyera kudzapemphera, sadzapindulapo kanthu.
13Awa ndi mau amene Yehova adanena za Moabu nthawi
zapitazo. 14Koma tsopano Yehova wanena, nati, Zisanapite zaka
zitatu monga zaka za wolembedwa nchito, ulemerero wa Moabu
udzakhala wonyozeka, ndi khamu lalikuru lace, ndi otsala
adzakhala ang'ongong'ono ndi acabe.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Aneneratu za Damasiko ndi Efraimu

1Katundu wa Damasiko. Taonani, Damasiko wacotsedwa
usakhalenso mudzi, ndimo udzangokhala muunda
wopasudwa. 2Midzi ya Aroeri yasiyidwa; idzakhala ya zoweta
zogona pansi, opanda woziopsya. 3Ku Efraimu sikudzakhalanso
linga, ngakhale ufumu ku Damasiko, ngakhale otsala kwa Aramu;
iwo adzakhala ngati ulemerero wa ana a Israyeli, ati Yehova
wamakamu.
4Ndipo padzakhala tsiku limenelo, kuti ulemerero wa Yakobo
udzakhala wopyapyala, ndi kunenepa kwa thupi lace
kudzaonda. 5Ndipo padzakhala ngati wamasika alikumweta tirigu
wosaceka, ndi dzanja lace lirikudula ngala; inde padzakhala ngati
pamene wina akunkha ngala m'cigwa ca Refaimu. 6Koma
mudzasiyidwa m'menemo khunkha, monga ngati kugwedeza
kwace kwa mtengo waazitona, zipatso ziwiri pena zitatu m'nsonga
ya nthambi yosomphoka, zinai pena zisanu m'nthambi za
kunthemba, za mtengo wobalitsa, ati Yehova, Mulungu wa
Israyeli. 7Tsiku limenelo munthu adzayang'ana kwa Mlengi wace,
ndipo maso ace adzalemekeza Woyera wa Israyeli. 8Ndipo iye
sadzayang'ana pa maguwa a nsembe, nchito ya manja ace,
ngakhale kulemekeza cimene anacipanga ndi zala zace, ngakhale
zifanizo pena mafano a dzuwa. 9Tsiku limenelo midzi yace yolimba
idzakhala ngati mabwinja a m'nkhalango, ndi a pansonga pa phiri,
osiyidwa pamaso pa ana a Israyeli; ndipo padzakhala
bwinja. 10Cifukwa iwe waiwala Mulungu wa cipulumutso cako,
sunakumbukira thanthwe la mphamvu zako; cifukwa cace iwe
waoka mitengo yokondweretsa, waokapo zipinjiri zacilendo; 11tsiku
lako looka uzingapo mpanda, nuphukitsa mbeu zako m'mawa
mwace; mulu wa masika udzaoneka tsiku lakulira ndi la cisoni
cothetsa nzeru.

Aneneratu za kufafanizika kwa nkhondo ya Asuri

12Ha, phokoso la mitundu yambiri ya anthu ambiri, amene apfuula
ngati kukukuma kwa nyanja: ndi kuthamanga kwa amitundu,
akuthamanga ngati kuthamangakwa madzi amphamvu! 13Mitundu
ya anthu idzathamanga ngati kuthamanga kwa madzi ambirimbiri;
koma Iye adzawadzudzula, ndipo iwo adzathawira patari,
nadzapitikitsidwa monga mankhusu a pamapiri patsogolo pa
mphepo, ndi monga pfumbi lokwetera patsogolo pa mkunthu wa
mphepo. 14Pa nthawi ya madzulo, taonani kuopsya; kusanace, iwo
palibe. Ili ndi gawo la iwo amene atifunkha ndi ici ciwagwera omwe
alanda zathu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Aneneratu za Etiopia

1Ha, dziko lakukupuza mapiko, liri tsidya lija la nyanja za
Etiopia; 2limene litumiza mithenga panyanja m'ngalawa
zatnabungwa zoyenda m'madzi, ndi kuti, Mukani, inu mithenga
yoyenda msanga msanga ku mtundu wa anthu atari ndi osalala,
kwa mtundu woopsya cikhalire cao, mtundu umene uyesa dziko
ndi kupondereza pansi, umene dziko lace nyanja
ziligawa! 3Inunonseakukhala m'dziko lapansi, ndi inu akukhazikika
pa dziko lapansi, potukulidwa cizindikiro pamwamba pa mapiri,
mudzaona, ndi polizidwa lipenga mudzamva. 4Pakuti Yehova
watero kwa ine, Ine ndidzakhala cete, ndipo ndidzayang'ana
mokhala cete, ndipo ndidzayang'ana mokhalamo Ine, monga
kuwala kotentha kwa dzuwa, monga mtambo wa mame
m'kutentha kwa masika. 5Pakuti masika asanafike, kutatha
kuphuka ndi posanduka duwa mphesa yofuna kucha, iye
adzadzombolera tinthambi ndi mphopo, ndi nthambi zotasa
adzazicotsa ndi kuzisadza. 6Adzasiyira mbalame zakulusa za
m'mapiri ndi zirombo za dziko nthambizo, ndipo mbalame zakulusa
zidzakhalapo m'dzinja, ndi zirombo zonse za dziko zidzakhalapo
m'malimwe. 7Nthawi imeneyo mphatso idzaperekedwa kwa Yehova
wa makamu, mtundu wa anthu atari ndi osalala, yocokera kwa
mtundu woopsya cikhalire cao; mtundu umene uyesa dziko ndi
kupondereza pansi, umene dziko lace nyanja ziligawa, ku malo a
dzina la Yehova wa makamu, phiri la Ziyoni.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Aneneratu za Aigupto

1Katundu wa Aigupto.
Taonani, Yehova wakwera pamwamba pa mtambo wothamanga,
nadza ku Aigupto; ndi mafano a Aigupto adzagwedezeka pakufika
kwace, ndi mtima wa Aigupto udzasungunuka pakati pace. 2Ndipo
ndidzapikisanitsa Aaigupto; ndipo adzamenyana wina ndi mbale
wace, ndi wina ndi mnansi wace; mudzi kumenyana ndi mudzi, ndi
ufumu kumenyana ndi ufumu. 3Ndipo mzimu wa Aigupto
adzakhala wacabe pakati pace; ndipo Ine ndidzaononga uphungu
wace; ndimo iwo adzafunafuna mafano ndi anyanga, ndi alauli, ndi
obwebweta. 4Ndipo ndidzapereka Aigupto m'manja mwa mbuye
wankharwe; ndi mfumu yaukali idzawalamulira, ati Ambuye,
Yehova wa makamu. 5Ndipo madzi adzaphwa m'nyanja yaikuru,
ndipo nyanja yoyendamo madzi idzaphwa, niuma. 6Ndipo nyanja
zidzanunkha; mitsinje ya Aigupto idzacepa, niuma; bango ndi
mlulu zidzafota. 7Madambo ovandikana ndi Nile, pafupi ndi gombe
la Nile, ndi zonse zobzyala pa Nile zidzauma, nizicotsedwa,
zosakhalanso konse. 8Asodzinso adzalira, ndi onse oponya mbedza
m'Nile adzaliralira, ndi onse oponya makoka m'madzi,
adzalefuka. 9Komanso iwo amene agwira nchito yakupala bwazi,
ndi iwo amene aomba nsaru yoyera, adzakhala ndi
manyazi. 10Ndipo maziko ace adzasweka, onse amene agwira
nchito yolipidwa adzabvutidwa mtima. 11Akalonga a Zoani apusa
ndithu; uphungu wa aphungu anzeru a Farao wasanduka
wopulukira; bwanji iwe unena kwa Farao, Ine ndine mwana wa
anzeru, mwana wa mafumu akale? 12Nanga tsopano anzeru ali
kuti? akuuze iwe tsopano; adziwe cimene Yehova wa makamu
watsimikiza mtima kucitira Aigupto. 13Akalonga a Zoani apusa,
akalonga a Nofi anyengedwa; iwo asoceretsa Aigupto, amene ali
mwala wa pangondya wa mapfuko ace. 14Yehova wasanganiza
mzimu wa kusaweruzika pakati pace; ndipo iwo asoceretsa Aigupto
m'nchito zonse zace, monga mwamuna woledzera ayenda
punzipunzi posanza pace. 15Aigupto sadzakhala ndi nchito, imene
mutu pena mcira, pena nthambi ya kanjedza, pena mlulu
zidzaigwira.
16Tsiku limenelo Aigupto adzanga akazi; ndipo adzanthunthumira
ndi kuopa, cifukwa ca kugwedeza kwa dzanja la Yehova wa
makamu, limene Iye agwedeza pamwamba pace. 17Ndipo dziko la
Yuda lidzaopsa Aigupto, yense wakulichula adzamtembenukira
mwamantha, cifukwa ca uphungu wa Yehova wa makamu,
aupanga pa dzikolo.

18Tsiku limenelo padzakhala midzi isanu m'dziko la Aigupto
yolankhula cinenero ca Kanani, ndi yolumbira, Pali Yehova wa
makamu; wina udzachedwa, Mudzi wa cionongeko.
19Tsiku limenelo padzakhala guwa la nsembe la Yehova pakati pa
dziko la Aigupto, ndi coimiritsa ca Yehova m'malire ace. 20Ndipo
cidzakhala cizindikiro ndi mboni ya Yehova wa makamu m'dziko la
Aigupto; pakuti iwo adzalirira kwa Yehova, cifukwa ca osautsa,
ndipo Iye adzawatumizira mpulumutsi, ndi wamphamvu,
nadzawapulumutsa. 21Ndipo Yehova adzadziwika kwa Aigupto,
ndipo Aaigupto adzadziwa Yehova tsiku limenelo; inde iwo
adzapembedzera ndi nsembe ndi zopereka, nadzawindira Yehova
ndi kucitadi. 22Ndipo Yehova adzakantha Aigupto kukantha ndi
kuciritsa; ndipo iwo adzabwerera kwa Yehova, ndipo Iye
adzapembedzedwa ndi iwo, nadzawaciritsa.
23Tsiku limenelo padzakhala khwalala locokera m'Aigupto kunka ku
Asuri, ndipo M-asuri adzafika ku Aigupto, ndi M-aigupto adzafika ku
Asuri, ndipo Aaigupto adzapembedzera pamodzi ndi Aasuri.
24Tsiku limenelo Israyeli ndi Aigupto ndi Asuri atatuwa, adzakhala
mdalitso pakati pa dziko lapansi; 25pakuti Yehova wa makamu
wadalitsa iwo, ndi kuti, Odalitsika Aigupto anthu anga, ndi Asuri
nchito ya manja anga, ndi Israyeli colowa canga.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Cizindikilo cakutyoka Aigupto ndi Etiopia

1Caka cimene kazembe wa ku Asuri anafika ku Asidodi, muja
Sarigoni mfumu ya Asuri anamtumiza iye, ndipo iye anamenyana
ndi Asidodi, naugonjetsa. 2Nthawi imeneyo Yehova ananena ndi
Yesaya, mwana wa Amozi, nati, Muka numasule ciguduli m'cuuno
mwako, nucicotse, nubvule nsapato yako ku phazi lako. Ndipo iye
anatero, nayenda marisece, ndi wopanda nsapato, 3Ndipo Yehova
anati, Monga mtumiki wanga Yesaya wayenda marisece ndi
wopanda nsapato zaka zitatu, akhale cizindikilo ndi codabwitsa
kwa Aigupto ndi kwa Etiopia; 4momwemo mfumu ya Asuri
idzatsogolera kwina am'nsinga a Aigupto, ndi opitikitsidwa a
Etiopia, ana ndi okalamba, amarisece ndi opanda nsapato, ndi
matako osabvala, kuti acititse manyazi Aigupto. 5Ndipo iwo
adzakhala ndi mantha ndi manyazi, cifukwa ca Kusi, amene
anawatama, ndi Aigupto, amene anawanyadira. 6Ndipo wokhala
m'mphepete mwa nyanja muno adzati tsiku limenelo, Taonani,
kuyembekeza kwathu kuli kotero, kumene ife tinathawira
atithangate kupulumutsidwa kwa mfumu ya Asuri, ndipo ife
tidzapulumuka bwanji?

©The Bible Society of Malawi, 1992

Aneneratu za kugwa kwa Babulo

1Katundu wa cipululu ca kunyanja. Monga akabvumvulu a kumwela
apitirira, kufumira kucipululu ku dziko loopsya. 2Masomphenya
obvuta aonetsedwa kwa ine; wogula malonda wonyenga
amangonyenga, ndi wofunkha amangofunkha. Kwera Elamu iwe;
zunguniza Media iwe; kuusa moyo kwace konse
ndakutonthoza. 3Cifukwa cace m'cuuno mwanga mwadzazidwa ndi
zopota; zopweteka zandigwira ine monga zopweteka za mkazi
pobala mwana; zowawa zindiweramitsa, makutu anga sangathe
kumva; ndicita mantha sindingathe kuona. 4Mtima wanga
uguguda, mantha andiopsetsa ine; cizitezite cimene
ndinacikhumba candisandukira kunthunthumira. 5Iwo akonza pa
gome lodyera, aika alonda, adya, namwa; ukani, akalonga inu,
dzozani mafuta cikopa. 6Pakuti Ambuye atero kwa ine, Muka, ika
mlonda anene cimene aciona; 7ndipo pamene iye anaona khamu,
amuna apakavalo awiri awiri, khamu la aburu, khamu la ngamila,
iye adzamvetsera ndi khama mosamalitsa. 8Ndipo iye anapfuulitsa
ngati mkango, Ambuye inu, ine ndiimabe pamwamba pa nsanja
nthawi ya usana, ndipo ndiikidwa mu ulonda wanga usiku
wonse; 9ndipo taonani, kuno kulinkudza khamu la amuna,
apaakavalo awiri awiri. Ndipo iye anayankha nati, Babulo wagwa,
wagwa; ndi mafano onse osema a milungu yace asweka, nagwa
pansi. 10Kuomba kwanga nanga, ndi za pa dwale langa: cimene ine
ndinacimva kwa Yehova wa makamu Mulungu wa Israyeli, ndanena
kwa inu.

Aneneratu za kuonongeka kwa Duma

11Katundu wa Duma.
Wina aitana kwa ine kucokera ku Seiri, Mlonda, nthawi yanji ya
usiku? Mlonda, nthawi yanji ya usiku? 12Mlonda anati, Kuli kuca,
koma kukali usiku; mukafuna kufunsa, funsani, bwerani, idzani.

Za kuonongeka kwa Arabiya

13Katundu wa pa Arabiya.
M'nkhalango ya m'Arabiya mudzagona, inu makamu oyendayenda
a Dedani. 14Mucingamire akumva ludzu ndi madzi; okhala m'dziko
la Tema ananka kukomana ndi othawa ndi cakudya cao. 15Pakuti
iwo anathawa malupanga, malupanga osololedwa, ndi mauta-
olifuka ndi nkhondo yobvuta. 16Pakuti Ambuye ana tero kwa ine,
Cisanapite caka malinga ndi zaka za wolembedwa nchito
ulemerero wonse wa Kedara udzagoma; 17ndi otsala amauta,
ngwazi za ana a Kedara zidzacepa, pakuti Yehova Mulungu wa
Israyeli wanena.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Aneneratu za kumangidwa misasa Yerusalemu

1Katundu wa cigwa ca masomphenya.
Mwatani kuti mwakwera nonsenu pamacindwi? 2Iwe amene
wadzala ndi zimpfuu, mudzi waphokoso, mudzi wokondwa;
ophedwa ako, sanaphedwa ndi lupanga, sanafe
m'nkhondo. 3Olamulira ako onse athawa pamodzi, anamangidwa
ndi amauta; opezedwa ako onse anamangidwa pamodzi, nathawira
patari. 4Comweco ndinati, Usandiyang'ane ine, ndilira ndi kuwawa
mtima; usafulumire kunditonthoza ine, cifukwa ca kufunkhidwa
kwa mwana wamkazi wa anthu anga, 5Pakuti ndi tsiku laphokoso,
ndi lopondereza pansi, ndi lothetsa nzeru, locokera kwa Ambuye
Yehova wa makamu, m'cigwa ca masomphenya, kugumuka kwa
malinga, ndi kupfuulira kumapiri. 6Ndipo Elamu anatenga phodo,
ndi magareta a anthu ndi apakavalo; ndipo Kiri anaonetsa
zikopa. 7Ndipo panali kuti zigwa zako zosankhika zinadzala
magareta, ndi apakavalo anadzinika okha pacipata. 8Ndipo Iye
anacotsa cophimba ca Yuda; ndipo iwe unayang'ana tsiku limenelo
pa zida za m'nyumba ya nkhalango. 9Ndipo inu munaona kuti pa
mudzi wa Davide panagumuka mipata yambiri; ndipo
munasonkhanitsa pamodzi madzi a m'thamanda lakunsi. 10Ndipo
inu munawerenga nyumba za Yerusalemu, ndipo munagwetsa
nyumba, kuti mumangire linga. 11Inu munapanganso cosungamo
madzi a thamanda lakale, pakati pa malinga awiri; koma inu
simunamuyang'ane iye amene anacicita ico, ngakhale kusamalira
iye amene analipanga kale. 12Ndipo tsiku limenelo Ambuye,
Yehova wa makamu, anaitana kulira, ndi kugwa misozi, ndi
kumeta, ndi kubvala ciguduli m'cuuno; 13koma taonani, kukondwa,
ndi kusekerera, ndi kupha ng'ombe, ndi kupha nkhosa, ndi kudya
nyama, ndi kumwa vinyo; tiyeni tidye ndi kumwa, cifukwa mawa
tidzafa. 14Ndipo Yehova wa makamu wadzibvumbulutsa yekha
m'makutu mwanga, Ndithu coipa cimeneci sicidzacotsedwa pa inu
kufikira inu mudzafa, ati Ambuye, Yehova wa makamu.

Kulangidwa kwa Sebina, kukuzidwa kwa Eliakimu

15Atero Ambuye Yehova wa makamu, Muka, pita iwe kwa kapitao
uyu, kwa Sebina woyang'anira nyumba, ndi kuti, 16Ucitanji iwe
kuno, ndimo ndani ali nawe kuno, kuti iwe wagoba manda kuno,
ndi kudzigobera manda pamwamba, ndi kudzisemera mogonamo
m'thanthwe. 17Taona Yehova adzakuponya iwe zolimba, monga
mwamuna wamphamvu, inde adzakufumbata zolimba. 18Iye ndithu
adzakuzunguza, ndi kukuponyaponya ngati mpira m'dzido lalikuru;
kumeneko iwe udzafa, ndipo kumeneko kudzakhala magareta a
ulemerero wako, iwe wocititsa manyazi banja la mbuye
wako. 19Ndipo Ine ndidzakuturutsa iwe mu nchito yako, ndi

kukutsitsa iwe pokhala pako. 20Ndipo padzakhala tsiku limenelo,
kuti ine ndidzaitana mtumiki wanga, Eliakimu mwana wa
Hilikiya: 21ndipo ndidzambveka iye cobvala cako, ndi kumlimbikitsa
ndi lamba lako, ndipo ndidzapereka ulamuliro wako m'dzanja lace;
ndipo iye adzakhala atate wa okhala m'Yerusalemu ndi a nyumba
ya Yuda. 22Ndipo ndidzaika mfungulo wa nyumba ya Davide
paphewa pace, ndipo iye adzatsegula, ndipo palibe wina
adzatseka, iye adzatseka ndipo palibe wina adzatsegula. 23Ndipo
ndidzamkhomera iye ngati msomali polimba; ndipo iye adzakhala
mpando wa ulemerero wa banja la atate wace. 24Ndipo iwo
adzapacika pa iye ulemerero wonse wa banja la atate wace,
obadwa ndi ana, mbiya zonse zazing'ono, ngakhale zikho ndi
aguda omwe. 25Tsiku limenelo, ati Yehova wa makamu, msomali
wokhomeredwa polimba udzasukusika; nudzaguluka, ndi kugwa,
ndi katundu wopacikidwapo adzadulidwa; pakuti Yehova wanena.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Kupasuka ndi kumangidwanso kwa Turo

1Katundu wa Turo.
Kuwani, inu ngalawa za Tarisi; cifukwa wapasudwa, kulibenso
nyumba, kulibe polowera; kucokera ku dziko la Kitimo
kwabvumbulutsidwa kwa iwo. 2Khalani cete, inu okhala
m'cisumbu; iwe amene anakudzazanso amalonda a ku Zidoni,
opita m'nyanja. 3Ndi pa nyanja zazikuru anapindula ndi mbeu za ku
Sihori ndizo dzinthu za ku Nile; ndi kumeneko kunali msika wa
amitundu. 4Khala ndi manyazi, iwe Zidoni; cifukwa nyanja yanena,
linga la kunyanja, ndi kuti, Ine sindinamve zowawa, kapena kubala,
kapena kulera anyamata, kapena kulera anamwali. 5Pofika mbiriyo
ku Aigupto, iwo adzamva kuwawa kwambiri pa mbiri ya
Turo. 6Olokani inu, kunka ku Tarisi, kuwani, inu okhala
m'cisumbu. 7Kodi umene ndi mudzi wanu wokondwa, wacikhalire
kale lomwe, umene mapazi ace anaunyamula kunka nao kutari
kukhalako? 8Ndani wapanga uphungu uno pa Turo, mudzi umene
upereka akorona, amalonda ace ali akalonga, ogulitsa ace ali
olemekezeka pa dziko lapansi? 9Yehova wa makamu wapanga
uphungu uwu, kuipitsa kunyada kwa ulemerero wonse, kupepula
onse olemekezeka a m'dziko lapansi. 10Pita pakati pa dziko lako
monga Nile, iwe mwana wamkazi wa Tarisi; palibenso lamba. 11Iye
watambasula dzanja lace panyanja, wagwedeza maufumu; Yehova
walamulira za amalonda, kupasula malinga ace. 12Ndipo Iye anati,
Iwe sudzakondwanso konse, iwe namwali wobvutidwa,
mwanawamkazi wa Zidoni; uka, oloka kunka ku Kitimu; ngakhale
kumeneko iwe sudzapumai. 13Taonani, dziko la Akasidi; anthu awa
sakhalanso; Asuri analiika ilo likhale la iwo okhala m'cipululu; iwo
amanga nsanja zao, nagumula nyumba za mafumu ace;
nalipasula. 14Kuwani, inu ngalawa za Tarisi; pakuti linga lanu
lapasulidwa. 15Ndipo padzakhala tsiku limenelo, kuti Turo
adzaiwalika zaka makumi asanu ndi awiri, malinga ndi masiku a
mfumu imodzi; zitapita zaka makumi asanu ndi ziwirizo, cidzakhala
kwa Turo monga m'nyimbo ya mkazi wadama. 16Tenga mngoli,
yendayenda m'mudzi, iwe mkazi wadama, amene unaiwalika;
yimba zokoma, curukitsa nyimbo, kuti ukumbukiridwe. 17Ndipo
padzali, zitapita zaka makumi asanu ndi awirizo, kuti Yehova
adzazonda Turo, ndipo iye adzabwerera ku mphotho yace,
nadzacita dama ndi maufumu onse a dziko lapansi, okhala kunja
kuno. 18Malonda ace ndi mphotho yace zidzakhala zopatulikira
Yehova; sizidzasungidwa kapena kuikidwa; cifukwa malonda ace
adzakhala kwa iwo, amene akhala pamaso pa Yehova, kuti adye
mokwana, nabvale caulemu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Cilango ca Mulungu ca pa dziko la Israyeli, ndi pa dziko lonse lapansi

1Taonani, Yehova apululutsa dziko, nalipasula, nalitembenuza
dodolido, nabalalitsa okhalamo ace. 2Ndipo padzakhala monga ndi
anthu, moteronso ndi ansembe; monga ndi mtumiki, moteronso
ndi mbuyace; monga ndi mdzakazi, moteronso ndi mbuyace
wamkazi; monga ndi wogula, moteronso ndi wogulitsa; monga ndi
wobwereka, moteronso ndi wombwereka; monga ndi wotenga
phindu, moteronso ndi wombwezera phindu kwa iye. 3Dziko
lidzapululuka konse, ndi kupasulidwa ndithu; pakuti Yehova
ananena mau amenewa. 4Dziko lilira nilifota, dziko lilefuka nilifota,
anthu omveka a padziko alefuka. 5Dzikonso laipitsidwa ndi
okhalamo ace omwe, cifukwa iwo alakwa pamalamulo
nasinthanitsa malemba, natyola cipangano ca nthawi
zonse. 6Cifukwa cace citemberero cadya dziko, ndi amene akhala
m'menemo apezedwa ocimwa, cifukwa cace okhalamo a padziko
atenthedwa, ndipo anthu owerengeka atsala. 7Vinyo watsopano
alira, mpesa ulefuka, mitima yonse yokondwa iusa
moyo. 8Kusangalala kwa mangaka kwalekeka, phokoso la iwo
amene aserera litha, kukondwa kwa mngoli kwalekeka. 9Iwo
sadzamwa vinyo ndi kuyimba nyimbo; cakumwa caukali cidzawawa
kwa iwo amene acimwa. 10Mudzi wosokonezeka wagwetsedwa
pansi; nyumba zonse zatsekedwa, kuti asalowemo munthu. 11Muli
mpfuu m'makwalala cifukwa ca vinyo; kukondwa konse
kwadetsedwa, kusangalala kwa dziko kwatha. 12M'mudzi mwatsala
bwinja, ndi cipata camenyedwa ndi cipasuko. 13Cifukwa cace
padzakhala cotero pakati pa dziko mwa anthu, ngati kugwedeza
kwa mtengo waazitona, ngati khunkha la mphesa, pakutha masika
ace. 14Amenewa adzakweza mau ao, nadzapfuula; cifukwa ca
cifumu ca Yehova, iwo adzapfuula zolimba panyanja. 15Cifukwa
cace lemekezani inu Yehova kum'mawa, ngakhale dzina la Yehova,
Mulungu wa Israyeli, m'zisumbu za m'nyanja.
16Kucokera ku malekezero a dziko ife tamva nyimbo zolemekeza
wolungama. Koma ine ndinati, Ndaonda ine, ndaonda ine, tsoka
kwa ine! amalonda onyenga amangonyenga; inde ogulitsa
onyenga apambana kunyenga. 17Mantha ndi dzenje ndi msampha
ziri pa iwe, wokhala m'dziko. 18Ndipo padzali, kuti iye amene
athawa mbiri yoopsya, adzagwa m'dzenje; ndi iye amene aturuka
m'kati mwa dzenje, adzakodwa mumsampha, pakuti mazenera a
kuthambo atsegudwa, ndi maziko a dziko agwedezeka. 19Dziko
lapansi lasweka ndithu, dziko lapansi lasungunukadi, dziko lapansi
liri kugwedezeka kopambana. 20Dziko lapansi lidzacita dzandi

dzandi, ngati munthu woledzera, ndi kunjenjemera, ngati cilindo;
ndi kulakwa kwace kudzalilemera, ndipo lidzagwa losaukanso.
21Ndipo padzali tsiku limenelo, kuti Yehova adzazonda kumwamba
khamu la kumwamba, ndi mafumu a dziko lapansi. 22Ndipo iwo
adzasonkhanitsidwa pamodzi, monga ndende zimasonkhanitsidwa
m'dzenje, ndi kutsekeredwa m'kaidi, ndipo atapita masiku ambiri
adzawazonda. 23Pompo mwezi udzanyazitsidwa, ndi dzuwa
lidzakhala ndi manyazi, pakuti Yehova wa makamu adzalamulira
caulemerero m'phiri la Ziyoni, ndi m'Yerusalemu, ndi pamaso pa
akuru akuru ace.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Nvimbo yakulemekeza cifundo ca Mulungu

1Yehova, Inu ndinu Mulungu wanga, ndidzakukuzani Inu,
ndidzatamanda dzina lanu, cifukwa mwacita zinthu zodabwitsa,
ngakhale: zauphungu zakale, mokhulupirika ndi
m'zoonadi. 2Cifukwa Inu mwasandutsa mudzi muunda; mudzi
walinga bwinja; nyumba ya alendo kuti isakhale mudzi;
sudzamangidwa konse. 3Cifukwa cace anthu amphamvu
adzakulemekezani Inu, mudzi wa mitundu yakuopsya udzakuopani
Inu. 4Cifukwa Inu mwakhala linga la aumphawi, linga la osowa
m'kubvutidwa kwace, pobisalira cimphepo, mthunzi wa pa dzuwa,
pamene kuomba kwa akuopsya kufanana ndi cimphepo cakuomba
chemba. 5Monga kutentha m'malo ouma, Inu mudzaletsa phokoso
la alendo; nyimbo ya akuopsya idzaletseka, monga mthunzi uletsa
dzuwa. 6Ndipo m'phiri limendi Yehova wa makamu adzakonzera
anthu ace onse phwando la zinthu zonona, phwando la vinyo wa
pamitsokwe, la zinthu zonona za mafuta okha okha, la vinyo
wansenga wokuntha bwino. 7Ndipo Iye adzaononga m'phiri
limeneli cophimba nkhope cobvundikira mitundu yonse ya anthu,
ndi nsaru yokuta amitundu onse. 8Iye wameza imfa ku nthawi
yonse; ndipo Ambuye Mulungu adzapukuta misozi pa nkhope
zonse; ndipo citonzo ca anthu ace adzacicotsa pa dziko lonse
lapansi; cifukwa Yehova wanena.
9Ndipo adzanena tsiku limenelo, Taonani, uyu ndiye Mulungu
wathu; tamlindirira Iye, adzatipulumutsa; uyu ndiye Yehova,
tamlindirira Iye, tidzakondwa ndikusekereram'cipulumutso
cace. 10Cifukwa m'phiri limeneli dzanja la Yehova lidzakhalamo,
ndipo Moabu adzaponderezedwa pansi m'malo ace, monga
maudzu aponderezedwa padzala. 11Ndipo iye adzatambasula
manja ace pakati pamenepo, monga wosambira atambasula manja
ace posambira; koma Iye adzagwetsa pansi kunyada kwace,
pamodzi ndi kunyenga kwa manja ace. 12Ndipo linga la pamsanje
la macemba ako Iye waligwetsa, naligonetsa pansi, nalifikitsa
padothi, ngakhale papfumbi.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Nyimbo yakulemekeza kuciniiriza kwa Yehova

1Tsiku limenelo adzayimba nyimbo imeneyi m'dziko la Yuda, Ife tiri
ndi mudzi wolimba; Iye adzaikacipulumutso cikhale macemba ndi
malinga. 2Tsegulani pazipata, kuti mtundu wolungama, umene
ucita zoonadi, ulowemo. 3Inu mudzasunga mtima wokhazikika mu
mtendere weni weni, cifukwa ukukhulupirirani Inu. 4Khulupirirani
Yehova nthawi zamuyaya, pakuti mwa Ambuye Yehova muli
thanthwe lacikhalire. 5Cifukwa Iye watsitsira pansi iwo amene
anakhala pamwamba, mudzi wa pamsanje; Iye wautsitsa,
wautsitsira pansi; waugwetsa pansi pa pfumbi. 6Phazi
lidzaupondereza pansi; ngakhale mapazi a aumphawi, ndi
mapondedwe a osowa. 7Njira ya wolungama iri njira yoongoka; Inu
amene muli woongoka, mukonza njira ya wolungama. 8Inde m'njira
ya maweruziro anu, Yehova, ife talindira Inu; moyo wathu ukhumba
dzina lanu, ndi cikumbukilo canu. 9Ndi moyo wanga ndinakhumba
Inu usiku; inde ndi mzimu wanga wa mwa ine ndidzafuna Inu
mwakhama; pakuti pamene maweruziro anu ali pa dziko lapansi,
okhala m'dziko lapansi adzaphunzira cilungamo. 10Ungayanje
woipa, koma sadzaphunzira cilungamo; m'dziko la macitidwe
oongoka, iye adzangocimwa, sadzaona cifumu ca Yehova.
11Yehova, dzanja lanu litukulidwa, koma iwo saona; koma iwo
adzaona cangu canu ca kwa anthu, nadzakhala ndi manyazi; inde
moto udzamariza adani anu. 12Yehova, udzatikhazikitsira
mtendere; pakuti mwatigwirira nchito zathu zonse. 13Yehova
Mulungu wathu, pamodzi ndi Inu ambuye ena adatilamulira ife;
koma mwa Inu nokha tidzachula dzina lanu. 14Iwo afa, atha,
sadzakhalanso ndi moyo; ali mizimu, sadzauka; cifukwa cace Inu
munawazonda, ndi kuwaononga, mwathetsa cikumbukiro cao
conse. 15Mwacurukitsa mtundu, Yehova, mwacurukitsa mtundu;
Inu mwalemekezeka, mwakuza malire onse a dziko.
16Yehova, iwo adza kwa Inu mobvutika, iwo anathira pemphero,
muja munalikuwalanga. 17Monga ngati mkazi wokhala ndi pakati,
amene nthawi yace yakubala yayandikira, amva zopweteka, ndi
kupfuula m'zowawa zace; momwemo takhala ife pamaso panu,
Yehova. 18Ife tinali ndi pakati, ife tinamva zopweteka, tafanana
ngati tabala mphepo; sitinacite cipulumutso ciri conse pa dziko
lapansi; ngakhale okhala m'dziko lapansi sanagwe. 19Akufa anu
adzakhala ndi moyo; mitembo yao idzauka. Ukani muyimbe, inu
amene mukhala m'pfumbi; cifukwa mame ako akunga mame a
pamasamba, ndipo dziko lapansi lidzaturutsa mizimu.
20Idzani, anthu anga, lowani m'zipinda mwanu, nimutseke
pamakomo panu; nimubisale kanthawi kufikira mkwiyo
utapita. 21Pakuti taonani, Yehova adza kucokera ku malo ace

kudzazonda okhala pa dziko lapansi, cifukwa ca kuipa kwao; dziko lidzabvumbulutsa mwazi wace, ndipo silidzabvundikiranso ophedwa ace.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Munda wamphesa wa Yehova

1Tsiku limenelo Yehova ndi lupanga lace lolimba ndi lalikuru ndi
lamphamvu adzalanga nangumi njoka yotamanga, ndi nangumi
njoka yopindika-pindika; nadzapha cing'ona cimene ciri m'nyanja.
2Tsiku limenelo: munda wa mphesa wavinyo, yimbani inu za
uwo. 3Ine Yehova ndiusunga uwo; ndidzauthirira madzi nthawi
zonse; ndidzausunga usiku ndi usana, kuti angauipse. 4Ndiribe
ukali; ndani adzalimbanitsa lunguzi ndi minga ndi Ine kunkhondo?
ndiziponde ndizitenthe pamodzi. 5Kapena mlekeni, agwire
mphamvu zanga, nacite nane mtendere; inde, acite nane
mtendere. 6M'mibadwo ikudzayo Yakobo adzamera mizu; Israyeli
adzaphuka ndi kucita mphundu; ndipo iwo adzadzaza ndi zipatso
pa dziko lonse lapansi.
7Kodi Mulungu wakantha Yakobo, monga umo anawakanthira
akumkanthawo? kapena kodi iye waphedwa malinga ndi kuphedwa
kwa iwo amene anaphedwa ndi iye? 8Munalimbana naye pang'ono,
pamene munamcotsa; wamcotsa iye kuomba kwace kolimba tsiku
la mphepo yamlumbanyanja. 9Cifukwa cace, mwa ici coipa ca
Yakobo cidzafafanizidwa, ndipo ici ndi cipatso conse cakucotsa
cimo lace; pamene iye adzayesa miyala yonse ya guwa la nsembe,
ngati miyala yanjeresa yoswekasweka, zifanizo ndi mafano a
dzuwa sizidzaukanso konse. 10Pakuti mudzi wocingidwa uli pa
wokha, mokhalamo mwa bwinja, ndi mosiyidwa ngati cipululu;
mwana wa ng'ombe adzadya kumeneko, nadzagonako pansi,
nadzamariza nthambi zace. 11Ponyala nthambi zace
zidzatyoledwa; akazi adzafika, nazitentha ndi moto, pakuti ali
anthu opanda nzeru; cifukwa cace Iye amene anawalenga
sadzawacitira cisoni, ndi Iye amene anawaumba sadzawakomera
mtima.
12Ndipo padzakhala tsiku limenelo, kuti Yehova adzaomba tirigu
wace, kucokera madzi a nyanja, kufikira ku mtsinje wa Aigupto,
ndipo mudzakunkhidwa mmodzi, inu ana a Israyeli.
13Ndipo padzakhala tsiku limenelo, lipenga lalikuru lidzaombedwa;
ndipo adzafika omwe akadatayika m'dziko la Asuri, ndi
opitikitsidwa a m'dziko la Aigupto; ndipo adzapembedza Yehova
m'phiri lopatulika la pa Yerusalemu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Kulangidwa kwa Efraimu ndi Yuda cifukwa ca kuuma mtima kwao

1Tsoka kwa korona wakunyada wa oledzera a Efraimu, ndi kwa
duwa lakufota la ulemerero wace wokongola, limene liri pamutu
paiwo, amene agwidwa ndi vinyo, m'cigwa ca nthaka
yabwino. 2Taonani, Ambuye ali ndi wina wamphamvu wolimba;
ngati cimphepo ca matalala, mkuntho wakuononga, ngati
namondwe wa madzi amphamvu osefukira, adzagwetsa pansi ndi
dzanja lamphamvu. 3Korona wakunyada wa oledzera a Efraimu
adzaponderezedwa; 4ndi duwa lakufota la ulemerero wace
wokongola, limene liri pamutu pa cigwa ca nthaka yabwino,
lidzakhala ngati nkhuyu yoyamba kuca malimwe asanafike; polona
wakupenya imeneyo, amaidya iri m'dzanja lace. 5Tsiku limenelo
Yehova wa makamu adzakhala korona wa ulemerero, ndi korona
wokongola kwa anthu ace otsala: 6ndipo adzakhala mzimu wa
ciweruziro kwa oweruza mirandu, ndi mphamvu kwa iwo amene
abweza nkhondo pacipata. 7Koma iwonso adzandima ndi vinyo,
nasocera ndi cakumwa caukali, wansembe ndi mneneri adzandima
ndi cakumwa caukali, iwo amezedwa ndi vinyo, nasocera ndi
cakumwa caukali, adzandima popenya, napunthwa
poweruza. 8Pakuti magome onse adzazidwa ndi masanzi ndi udio,
palibe malo okonzeka. 9Kodi Mulungu adzaphunzitsa yani nzeru?
Kodi Iye adzamvetsa yani uthengawo? iwo amene aletsedwa
kuyamwa, nacotsedwa pamabere? 10Pakuti pali langizo ndi langizo,
langizo ndi langizo; lamulo ndi lamulo, lamulo ndi lamulo; kuno
pang'ono, uko pang'ono. 11Iai, koma ndi anthu a milomo yacilendo,
ndi a lilume lina, Iye adzalankhula kwa anthu awa; 12amene
ananena nao, Uku ndi kupuma, mupumitsa wolema, ndi apa ndi
potsitsimutsa, koma iwo anakana kumva. 13Cifukwa cace mau a
Yehova adzakhala kwa iwo langizo ndi langizo, langizo ndi langizo;
lamulo ndi lamulo, lamulo ndi lamulo; kuno pang'ono, uko
pang'ono; kuti ayende ndi kugwa cambuyo, ndi kutyoka, ndi
kukodwa mumsampha, ndi kugwidwa.
14Cifukwa cace imvani mau a Yehova, inu amuna amnyozo,
olamulira anthu awa a m'Yerusalemu. 15Cifukwa inu munati, Ife
tapangana pangano ndi imfa, tabvomerezana ndi kunsi kwa
manda; pakuti mliri wosefukira sudzatifikira ife; pakuti tayesa
mabodza pothawirapo pathu, ndi kubisala m'zonyenga; 16cifukwa
cace Ambuye Yehova atero, Taonani, ndiika m'Ziyoni mwala wa
maziko, mwala woyesedwa mwala wa pangondya, wa mtengo
wace wokhazikika ndithu; wokhulupirira sadzafulumira. 17Ndipo
ndidzayesa ciweruziro cingwe coongolera, ndi cilungamo cingwe
colungamitsira ciriri; ndipo matalala adzacotsa pothawirapo

mabodza, ndi madzi adzasefukira mobisalamo. 18Ndipo pangano
lanu ndi imfa lidzathedwa, ndi kubvomerezana kwanu ndi kunsi
kwa manda kudzalepereka; popita mliri woopsya
udzakuponderezani pansi. 19Nthawi zonse umapita,
udzakutengani; cifukwa m'mawa ndi m'mawa udzapita, usana ndi
usiku; ndipo kudzakhala kuopsya kokha, kumva mbiri
yace. 20Pakuti kama wafupika, munthu sangatambalale pamenepo;
ndi copfunda cacepa, sicingamfikire. 21Pakuti Yehova adzauka
monga m'phiri la Perazimu, nadzakwiya monga m'cigwa ca
Gibeoni; kuti agwire nchito yace, nchito yace yacilendo, ndi kuti
acite cocita cace, cocita cace cacilendo. 22Tsono musakhale
amnyozo, kuti nsinga zanu zingalimbe; pakuti Ambuye, Yehova wa
makamu, wandimvetsa za cionongeko cotsimikizidwa pa dziko
lonse lapansi.
23Cherani inu makutu, imvani mau anga; mverani, imvani
kulankhula kwanga. 24Kodi mlimi amalimabe kuti abzale? kodi
amacocolabe, ndi kuswa zibuma za nthaka? 25Atakonza tyatyatya
pamwamba pace, kodi safesa ponse mawere, ndi kumwazamwaza
citowe, nafesa tirigu m'mizere ndi barele m'malo ace osankhika,
ndi mcewere m'maliremo? 26Pakuti Mulungu wace amlangiza
bwino namphunzitsa. 27Pakuti sapuntha mawere ndi copunthira
cakuthwa, ngakhale kuzunguniza njinga ya gareta pacitowe; koma
amakulunga mawere ndi munsi, naomba citowe ndi
cibonga. 28Tirigu wa mkate aperedwa; pakuti samampuntha
osaleka; ngakhale kuyendetsapo njinga ya gareta wace, ngakhale
kumphwanya ndi ziboda za akavalo ace sapera. 29Icinso cifumira
kwa Yehova wa makamu, uphungu wace uzizwitsa ndi nzeru yace
impambana.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Aneneratu za kulangidwa kwa Yuda wosakhulupirika, komanso za cipulumutso cace

1Eya Arieli, Arieli, mudzi umene Davide anamangapo zithando!
oniezerani caka ndi caka; maphwando afikenso; 2pamenepo
ndidzasautsa Arieli, ndipo padzakhala maliro ndi kulira; koma iye
adzakhala kwa Ine monga Arieli. 3Ndipo ndidzamanga zithando
kuzungulira iwe ponse, ndipo ndidzamanga linga ndi kuunjika
miulu yakumenyanirana ndi iwe. 4Ndipo iwe udzagwetsedwa pansi,
nudzanena uli pansi, ndi kulankhula kwako kudzakhala pansi
koturuka m'pfumbi; ndi mau ako adzakhala ngati a wina amene ali
ndi mzimu wobwebweta, kucokera pansi, ndi kulankhula kwako
kudzakhala konong'ona kocokera m'pfumbi, 5Koma khamu la
acilendo ako lidzafanana ndi pfumbi losalala, ndi khamu la oopsya
lidzakhala monga mungu wocokacoka; inde kudzaoneka
modzidzimuka dzidzidzi. 6Ndipo Yehova wa makamu adzamzonda
ndi bingu, ndi cibvomezi, ndi mkokomo waukuru, kabvumvulu, ndi
mkuntho, ndi lawi la moto wonyambita. 7Ndipo khamu la mitundu
yonse yomenyana ndi Arieli, ngakhale yonse yomenyana naye ndi
linga lace, ndi kumsautsa idzafanana ndi loto, masomphenya a
usiku. 8Ndipo kudzafanana ndi munthu wanjala, pamene alota,
ndipo, taonani, akudya; koma auka, ndipo m'kati mwace muli zi;
kapena monga munthu waludzu pamene alota, ndipo, taonani,
akumwa; koma auka ndipo taonani walefuka, ndipo m'kati mwace
muli gwa; momwemo lidzakhala khamu la mitundu yonse
yomenyana ndi phiri la Ziyoni.
9Khalani ndi kudabwa; sangalalani ndi kukhala akhungu; iwo
aledzera, koma si ndi vinyo, ali dzandi dzandi; koma si ndi
cakumwa caukali. 10Pakuti Yehova watsanulira pa inu mzimu wa
tulo togonetsa, natseka maso anu, ndiwo aneneri; naphimba mitu
yanu, ndiwo alauli. 11Ndipo masomphenya onse akusandukirani
mau a m'buku limatidwa ndi phula, limene anthu amapereka kwa
wina wodziwa kuwerenga, nati, Werengani umu; koma ati,
Sindingathe, cifukwa lamatidwa ndi phula; 12ndipo buku
laperekedwa kwa wosadziwa kuwerenga, ndi kuti, Werengani umu;
koma ati, Ine sindinaphunzira.
13Ndipo Ambuye anati, Popeza anthu awa ayandikira ndi Ine ndi
m'kamwa mwao, nandilemekeza ndi milomo yao, koma mtima wao
uli kutari ndi Ine, ndi mantha ao akundiopa Ine, ndi lamulo la anthu
analiphunzira; 14cifukwa cace, taonani, ndidzacitanso mwa anthu
awa nchito yodabwitsa, ngakhale nchito yodabwitsa ndi yozizwitsa;
ndipo nzeru ya anthu ao anzeru idzatha, ndi luntha la anthu ao
ozindikira lidzabisika.

15Tsoka kwa iwo amene afunitsa kubisira Yehova uphungu wao, ndi
nchito zao ziri mumdima, ndipo amati Ndani ationa ife? ndani
atidziwa ife? 16Ozolitsa inu! Kodi woumba adzayesedwa ngati
dothi; kodi cinthu copangidwa cinganene za iye amene
anacipanga, Iye sanandipanga ine konse; kapena kodi cinthu
coumbidwa cinganene za iye amene anaciumba, Iye alibe
nzeru? 17Kodi sikatsala kamphindi kakang'ono, ndipo Lebano
adzasanduka munda wobalitsa, ndi munda wobalitsa udzayesedwa
nkhalango? 18Ndipo tsiku limenelo gonthi adzam va mau a m'buku,
ndi maso akhungu adzaona poturuka m'zoziya ndi
mumdima. 19Ofatsanso kukondwa kwao kudzacuruka mwa Yehova,
ndi aumphawi a mwa anthu adzakondwerera mwa Woyera wa
Israyeli. 20Pakuti woopsya wagoma, ndi wonyoza watha, ndi onse
odikira zolakwa alikhidwa; 21amene apalamulitsa munthu mlandu,
namchera msampha iye amene adzudzula pacipata, nambweza
wolungama ndi cinthu cacabe. 22Cifukwa cace Yehova amene
anaombola Abrahamu, atero za banja la Yakobo: Yakobo
sadzakhala ndi manyazi tsopano, ngakhale nkhope yace tsopano
sidzagwa. 23Koma pamene iye aona ana ace, nchito ya manja
anga, pakati pa iye, iwo adzayeretsa dzina langa; inde, iwo
adzayeretsa Woyera wa Yakobo, nadzaopa Mulungu wa
Israyeli. 24Iwonso osocera mumzimu adzadziwa luntha, ndi iwo
amene ang'ung'udza adzaphunzitsidwa.

©The Bible Society of Malawi, 1992

1Tsoka okhulupirira Aigupto. Tsoka kwa ana opanduka, ati Yehova,
amene atenga uphungu koma si pa Ine; napangana pangano
opanda mzimu wanga, kuti aonjezere cimo ndi cimo; 2amene
ayenda kutsikira ku Aigupto, osafunsa kukamwa kwanga,
kudzilimbitsa iwo okha ndi li mphamvu za Farao, ndi kukhulupirira
mthunzi wa Aigupto 3Cifukwa cace mphamvu za Farao zidzakhala
kwa inu manyazi, ndi kukhulupirira mthunzi wa Aigupto kudzakhala
cisokonezo canu. 4Pakuti akalonga ace ali pa Zaani, ndi mithenga
yace yafika ku Hanesi. 5Iwo onse adzakhala ndi manyazi, ndi anthu
amene sangapindule nao kanthu, amene sakhala kwa iwo thangata,
pena phindu, koma manyazi ndi citonzo.
6Katundu wa zirombo za kumwera.
M'dziko lobvuta ndi lopweteka, kumeneko kucokera mkango
waukazi, ndi wamphongo, mphiri, ndi njoka youluka yamoto, iwo
anyamula cuma cao pamsana pa aburu, ndi ang'ono zolemera zao
pa malinundu a ngamila, kunka kwa anthu amene sadzapindula
nao. 7Pakuti thangata la Aigupto liri lacabe, lopanda pace; cifukwa
cace ndamucha wonyada, wokhala cabe. 8Tsopano pita, ukalembe
mauwa pamaso pao pathabwa, nuwalembe m'buku, kuti
akakhalebe ku nthawi yam'tsogolo, mboni ya masiku onse. 9Pakuti
ali anthu opanduka, ana onama, ana osafuna kumva cilamulo ca
Yehova; 10amene amati kwa alauli, Mtima wanu usapenye; ndi kwa
aneneri, Musanenere kwa ife zinthu zoona, munene kwa ife zinthu
zamyadi, munenere zonyenga; 11cokani inu munjira, patukani
m'bande, tiletsereni Woyera wa Israyeli pamaso pathu. 12Cifukwa
cace atero Woyera wa Israyeli, Popeza inu mwanyoza mau awa,
nimukhulupirira nsautso ndi mphulupulu, ndi kukhala
m'menemo; 13cifukwa cace kuipa kumeneku kudzakhala kwa inu
monga pogumuka pofuna kugwa, monga potukuka m'khoma
lalitari, kugumuka kwace kufika modzidzimutsa dzidzidzi. 14Ndipo
Iye adzagumulapo, monga mbiya ya woumba isweka, ndi
kuiswaiswa osaileka; ndipo sipadzapezedwa m'zigamphu zace
phale lopalira moto pacoso, ngakhale lotungira madzi
padziwe. 15Pakuti atero Ambuye, Yehova Woyera wa Israyeli,
M'kubwera ndi m'kupuma inu mudzapulumutsidwa; m'kukhala cete
ndi m'kukhulupirira mudzakhala mphamvu yanu; ndipo
simunafuna. 16Koma munati, Iai, pakuti tidzathawa pa akavalo;
cifukwa cace inu mudzathawadi; ndipo ife tidzakwera pa akavalo
aliwiro; cifukwa cace iwo amene akuthamangitsani, adzakhala
aliwiro. 17Cikwi cimodzi cidzathawa pakuwadzudzula mmodzi;
pakukudzudzulani anthu asanu mudzathawa; kufikira inu
mudzasiyidwa ngati mlongoti pamwamba pa phiri, ndi ngati
mbendera pamwamba pa citundu. 18Cifukwa cace Yehova

adzadikira, kuti akukomereni mtima, ndipo cifukwa cace Iye adzakuzidwa, kuti akucitireni inu cifundo; pakuti Yehova ndiye Mulungu wa ciweruziro; odala ali onse amene amdikira Iye.
19Pakuti anthu adzakhala m'Ziyoni pa Yerusalemu; iwe sudzaliranso, Iye ndithu adzakukomera mtima pakumveka kupfuula kwako; pakumva Iye adzayankha. 20Ndipo ngakhale Ambuye adzakupatsani inu cakudya ca nsautso, ndi madzi a cipsinjo, koma aphunzitsi ako sadzabisikanso, koma maso ako adzaona aphunzitsi ako; 21ndipo makutu ako adzamva mau kumbuyo kwa iwe akuti, Njira ndi iyi, yendani inu m'menemo: potembenukira inu kulamanja, ndi potembenukira kulamanzere. 22Ndipo mudzaipitsa cokuta ca mafano ako, osema asiliva, ndi comata ca mafano ako osungunula agolidi; udzawataya ngati kanthu konyansa, udzati kwa iwo, Cokani. 23Ndipo Mulungu adzapatsa mvula ya mbeu yako, ukaibzale m'nthaka; ndi mkate ndiwo phindu la nthaka, ndipo tirigu wace adzaca bwino ndi kucuruka; tsiku limenelo ng'ombe zako zidzadya m'madambo akuru. 24Momwemonso ng'ombe ndi ana a buru olima nthaka adzadya cakudya cocezera, cimene capetedwa ndi cokokolera ndi mkupizo. 25Ndipo pamwamba pa mapiri akuru onse, ndipa zitunda zonse zazitaritari padzakhala mitsinje ndi micerenje ya madzi, tsiku lophana lalikuru, pamene nsanja zidzagwa. 26Komanso kuwala kwace kwa mwezi kudzakhala ngati kuwala kwa dzuwa, ndi kuwala kwa dzuwa kudzakula monga madzuwa asanu ndi awiri, monga kuwala kwa masiku asanu ndi awiri, tsiku limenelo Yehova adzamanga bala la anthu ace, nadzapoletsa khana limene anawakantha ena.
27Taonani, dzina la Yehova licokera kutari, mkwiyo wace uyaka, malawi ace ndi akuru; milomo yace iri yodzala ndi ukali, ndi lilime lace liri ngati moto wonyambita; 28ndi mpweya wace uli ngati mtsinje wosefukira, umene ufikira m'khosi, kupeta mitundu ya anthu ndi copetera ca cionongeko; ndi capakamwa calakwitsa, cidzakhala m'nsagwada za anthu. 29Inu mudzakhala ndi nyimbo, monga usiku, podya phwando lopatulika; ndi mtima wokondwa, monga pomuka wina ndi citoliro, kufikira ku phiri la Yehova, ku thanthwe la Israyeli, 30Ndipo Yehova adzamveketsa mau ace a ulemerero, ndipo adzaonetsa kumenya kwa dzanja lace, ndi mkwiyo wace waukali, ndi lawi la moto wonyambita, ndi kuomba kwa mphepo, ndi mkuntho ndi matalala. 31Pakuti ndi mau a Yehova Asuri adzatyokatyoka, ndi ndodo yace adzammenya. 32Ndipo nthawi zonse Yehova adze vakantha ndi ndodo yosankhikayo, padzamveka mangaka ndi zeze; ndi m'nkhondo zothunyana-thunyana, Iye adzamenyana nao. 33Pakuti Tofeti wakonzedwa kale, inde cifukwa ca mfumu wakonzedweratu; Iye wazamitsapo,

nakuzapo; mulu wacewo ndi moto ndi nkhuni zambiri; mpweya wa Yehova uuyatsa ngati mtsinje wasulfure.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Toka otama cithandizo ca Aigupto

1Tsoka kwa iwo amene atsikira kunka ku Aigupto kukathandizidwa,
natama akavalo; nakhulupirira magareta, pakuti ali ambiri, ndi
okwera pa akavalo, pakuti ali a mphamvu zambiri; koma
sayang'ana Woyera wa Israyeli, ngakhale kumfuna Yehova! 2Koma
Iyenso ali wanzeru, nadzatengera coipa, ndipo sadzabwezanso
mau ace, koma adzaukira banja la ocita zoipa, ndi amene
athandiza iwo akugwira nchito yoipa. 3Koma Aaigupto ndiwo anthu,
si Mulungu; ndi akavalo ao ali nyama, si mzimu; ndipo pamene
Yehova adzatambasula dzanja lace, wothandiza adzapunthwa, ndi
wothandizidwa adzagwa, ndipo iwo onse awiri pamodzi
adzalephera. 4Pakuti Yehova atero kwa ine, Monga mkango, ndi
mwana wa mkango wobangula pa nyama yace, sudzaopa mau a
khamu la abusa oitanidwa kuupitikitsa, ngakhale kudzicepetsa
wokha, cifukwa ca phokoso lao; motero Yehova wa makamu
adzatsikira kumenyana nkhondo ku phiri la Ziyoni, ndi kucitunda
kwace komwe. 5Monga mbalame ziuluka, motero Yehova
wamakamu adzacinjiriza Yerusalemu; Iye adzacinjirikiza ndi
kuupulumutsa, adzapitirapo ndi kuusunga. 6Bwerani kwa Iye
amene mwampandukira kolimba, ana a Israyeli inu. 7Pakuti tsiku
limenelo iwo adzataya munthu yense mafano ace asiliva, ndi
mafano ace agolidi amene manja anu anu anawapanga
akucimwitseni inu. 8Pamenepo Asuri adzagwa ndi lupanga losati la
munthu; ndi lupanga losati la anthu lidzammariza iye; ndipo iye
adzathawa lupanga, ndi anyamata ace adzalamba. 9Ndipo mwala
wace udzacoka, cifukwa ca mantha, ndi akalonga ace adzaopa
mbendera, ati Yehova, amene moto wace uli m'Ziyoni, ndi ng'anjo
yace m'Yerusalemu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Ufumu wa mfumu yolungama

1Taonani mfumu idzalamulira m'cilungamo, ndi akalonga
adzalamulira m'ciweruzo. 2Ndipo munthu adzakhala monga
pobisalira mphepo, ndi pousira cimphepo; monga mitsinje yamadzi
m'malo ouma, monga mthunzi wa thanthwe lalikuru m'dziko
lotopetsa. 3Ndipo maso a iwo amene aona sadzatsinzina, ndi
makutu a iwo amene amva adzamvera. 4Mtimanso wansontho
udzadziwa nzeru, ndi lilume la acibwibwi lidzalankhula zomveka
msanga. 5Wopusa sadzayesedwanso woolowa manja, ngakhale
wouma manja sadzayesedwa mfulu. 6Pakuti wopusa adzanena
zopusa, ndi mtima wace udzacita mphulupulu, kucita zoipitsa, ndi
kunena za Yehova molakwira, kusowetsa konse mtima wanjala, ndi
kulepheretsa cakumwa ca waludzu. 7Zipangizonso za womana ziri
zoipa; iye apangira ziwembu zakuononga waumphawi ndi mau
onama, ngakhale pamene wosowa alankhula zoona. 8Koma mfulu
aganizira zaufulu, nakhazikika m'zaufulu zomwe.

Cilangizo ca kwa akazi

9Ukani, akazi inu, amene mulinkukhala phe, mumve mau anga; mu
ana akazi osasamalira, cherani makutu pa kulankhula
kwanga. 10Pakutha caka, kudza masiku ena inu mudzabvutidwa,
inu akazi osasamalira; pakuti masika a mphesa adzasoweka,
sadzatuta konse. 11Nthunthumirani, inu akazi, amene
mulinkukhalaphe; bvutidwani, inu osasamalira, bvulani mukhale
marisece, nimumange ciguduli m'cuuno mwanu. 12Iwo
adzadzimenya pazifuwa cifukwa ca minda yabwino, cifukwa ca
mpesa wobalitsa. 13Pa dziko la anthu anga padzafika minga ndi
lunguzi; inde pa nyumba zonse zokondwa, m'mudzi
wokondwerera; 14pakuti nyumba ya mfumu idzasiyidwa; mudzi wa
anthu ambiri udzakhala bwinja; citunda ndi nsanja zidzakhala
nkhwimba ku nthawi zonse, pokondwera mbidzi podyera
zoweta; 15kufikira mzimu udzathiridwa pa ife kucokera kumwamba,
ndi cipululu cidzasanduka munda wobalitsa, ndi munda wobalitsa
udzayesedwa nkhalango. 16Pamenepo ciweruzo cidzakhala
m'cipululu, ndi cilungamo cidzakhala m'munda wobalitsa. 17Ndi
nchito ya cilungamo idzakhala mtendere; ndi zotsata cilungamo
zidzakhala mtendere, ndi kukhulupirika ku nthawi zonse. 18Ndipo
anthu anga adzakhala m'malo a mtendere, ndi mokhala
mokhulupirika ndi mopuma mwa phe. 19Koma kudzagwa matalala
m'kugwa kwace kwa nkhalango; ndipo mudzi udzagwetsedwa
ndithu. 20Odala muli inu, amene mubzala m'mbali mwa madzi
monse, amene muyendetsa mapazi a ng'ombe ndi buru.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Adani a anthu a Mulungu adzapasuka; Yerusalemu adzabwezedwa ulemu

1Tsoka kwa iwe amene usakaza, cinkana sunasakazidwa;
nupangira ciwembu, cinkana sanakupangira iwe ciwembu! Utatha
kusakaza, iwe udzasakazidwa; ndipo utatha kupangira ciwembu,
iwo adzakupangira iwe ciwembu. 2Inu Yehova, mutikomere ife
mtima; ife talindira Inu; mukhale dzanja lathu m'mawa ndi
m'mawa, cipulumutso cathunso m'nthawi ya mabvuto. 3Pa mau a
phokoso mitundu ya anthu yathawa; ponyamuka iwe amitundu
abalalika, 4Ndipo zofunkha zanu zidzasonkhanitsidwa, monga
ziwala zisonkhana; monga madzombe atumpha, iwo adzatumpha
pa izo. 5Yehova wakwezedwa; pakuti akhala kumwamba; Iye
wadzaza Ziyoni ndi ciweruzo ndi cilungamo. 6Ndipo kudzakhala
cilimbiko m'nthawi zako, cipulumutso cambiri, nzeru ndi kudziwa;
kuopa kwa Yehova ndiko cumacace.
7Taonani, olimba mtima ao angopfuula kunja, mithenga ya
mtendere ilira kowawa. 8Njira zamakwalala zikufa, kulibe
woyendamo; Asuri watyola cipangano, wanyoza midzi, sasamalira
anthu. 9Dziko lilira maliro ndi kulefuka; Lebano ali ndi manyazi,
nafota; Saroni afanana ndi cipululu; pa Basana ndi Karimeli
papukutika. 10Tsopano ndidzauka, ati Yehova; tsopano
ndidzanyamuka, tsopano ndidzakwezedwa. 11Inu mudzatenga
pakati ndi mungu, mudzabala ziputu; mpweya wanu ndi moto
umene udzakumarizani inu. 12Ndipo mitundu ya anthu idzanga
potentha miyala yanjeresa; monga minga yodulidwa, nitenthedwa
ndi moto.
13Imvani inu amene muli kutari, cimene ndacita ndi inuamene muli
pafupi, bvomerezani mphamvu zanga, 14Ocimwa a m'Ziyoni ali ndi
mantha, kunthunthumira kwadzidzimutsa anthu opanda Mulungu.
Ndani mwa ife adzakhala ndi moto Wakunyeketsa? ndani mwa ife
adzakhala ndi zotentha zacikhalire? 15Iye amene ayenda
molungama, nanena molunjika; iye amene anyoza phindu
lonyenga, nasansa manja ace kusalandira zokometsera milandu,
amene atseka makutu ace kusamva za mwazi, natsinzina maso
ace kusayang'ana coipa; 16iye adzakhala pamsanje; malo ace
ocinjikiza adzakhala malinga amiyala; cakudya cace cidzapatsidwa
kwa iye; madzi ace adzakhala cikhalire. 17Maso ako adzaona
mfumu m'kukongola kwace; iwo adzaona dziko lakutari. 18Mtima
wako udzaganizira zoopsya; mlembi ali kuti? ali kuti iye amene
anayesa msonkho? ali kuti iye amene anawerenga nsanja? 19Iwe
sudzaona anthu aukali, anthu a mau anthulu, amene iwe
sungazindikire; a lilume lacibwibwi, limene iwe
sungalimve. 20Tayang'ana pa Ziyoni, mudzi wa mapwando athu;

maso ako adzaona Yerusalemu malo a phe, cihema cimene
sicidzasunthidwa, ziciri zace sizidzazulidwa konse, zingwe zace
sizidzadulidwa. 21Koma pamenepo Yehova adzakhala ndi ife
m'cifumu, malo a nyanja zacitando ndi mitsinje; m'menemo
ngalawa sizidzayenda ndi ngombo, ngakhale zombo zazikuru
sizidzapita pamenepo. 22Pakuti Yehova ndiye woweruza wathu,
Yehova ndiye wotipatsa malamulo, Yehova ndiye mfumu yathu; Iye
adzatipulumutsa. 23Zingwe zako za ngalawa zamasulidwa;
sizinathe kulimbitsa patsinde pa mlongoti wace, sizinathe
kufutukula matanga; pamenepo ndipo colanda cacikulu, cofunkha
cinagawanidwa; wopunduka nafumfula. 24Ndipo wokhalamo
sadzanena, Ine ndidwala; anthu okhala m'menemo,
adzakhululukidwa mphulupulu zao.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Yehova aipidwa ndi amitundu

1Idzani pafupi, amitundu inu, kuti mumve; mverani anthu inu,
dziko limve, ndi za mommo; dziko ndi zinthu zonse
zoturukamo. 2Pakuti Yehova akwiyira amitundu onse, nacitira ukali
khamu lao lonse; Iye wawaononga psiti, wawapereka
kukaphedwa, 3Ophedwa aonso adzatayidwa kunja, ndipo kununkha
kwa mitembo yao kudzamveka, ndipo mapiri adzasungunuka ndi
mwazi wao. 4Ndipo makamu onse a kumwamba adzasungunuka,
ndi miyamba idzapindika pamodzi ngati mpukutu; makamu ao
onse adzafota monga tsamba limafota pampesa ndi kugwa, ndi
monga tsamba lifota pamkuyu. 5Pakuti lupanga langa lakhuta
kumwamba; taonani, lidzatsikira pa Edomu, ndi pa anthu amene
ndawatemberera, kuti aweruzidwe. 6Lupanga la Yehova lakhuta ndi
mwazi, lanona ndi mafuta ndi mwazi wa ana a nkhosa, ndi mbuzi,
ndi mafuta a imso ya nkhosa zamphongo; pakuti Yehova ali ndi
nsembe m'Bozira, ndi ophedwa ambiri m'dziko la Edomu. 7Ndipo
njati zidzatsika ndi iwo, ndi ng'ombe zofula ndi zamphongo; ndi
dziko lao lidzakhuta ndi mwazi, ndi pfumbi lao lidzanona ndi
mafuta. 8Pakuti liri tsiku la kubwezera la Yehova, caka cakubwezera
cilango, mlandu wa Ziyoni. 9Ndipo mitsinjeyo idzasanduka matope
akuda, ndi pfumbilo lidzasanduka suifure, ndi dziko lacelo
lidzasanduka matope oyaka moto. 10Sadzazimikai usiku, ngakhale
usana; utsi wace udzakwera nthawi zonse; m'mibadwo mibadwo
lidzakhala labwinja, palibe amene adzapitapo nthawi za
nthawi. 11Koma bvuo ndi nungu zidzakhalamo, ndipo kadzidzi ndi
khungubwi adzakhala m'menemo, ndipo Mulungu adzatambalika
pamenepo cingwe coongolera ca cisokonezo, ndi cingwe
colungamitsa ciriri cosatha kucita kanthu. 12Iwo adzaitana mfulu
zace zilowe m'ufumu, koma sizidzaonekako; ndi akalonga ace onse
adzakhala cabe. 13Ndipo minga idzamera m'nyumba zace zazikuru,
khwisa ndi mitungwi m'malinga mwace; ndipo adzakhala malo a
ankhandwe, ndi bwalo la nthiwatiwa. 14Ndipo zirombo za
m'cipululu zidzakomana ndi mimbulu, tonde adzaitana mnzace;
inde mancici adzatera kumeneko, nadzapeza
popumira. 15Kumeneko njoka yotumpha idzapanga cisanja cace,
niikira, niumatira, niswa mumthunzi mwace; inde kumeneko
miimba idzasonkhana wonse ndi unzace. 16Funani inu m'buku la
Yehova, nimuwerenge; palibe umodzi wa iye udzasowa, palibe
umodzi udzasowa unzace; pakuti pakamwa pa Yehova panena,
ndipo mzimu wace wasonkhanitsa iwo. 17Ndipo Iye wacita maere,
cifukwa ca zirombozi, ndipo dzanja lace lazigawira dzikolo ndi
cingwe, zidzakhala nalo nthawi zonse ku mibadwo mibadwo,
zidzakhala m'menemo.

Cikondwerero ca Ziyoni m'tsogolomo

1Cipululu ndi malo ouma adzakondwa; ndipo dziko loti se
lidzasangalala ndi kuphuka ngati duwa. 2Lidzaphuka mocuruka ndi
kusangalala, ngakhale kukondwa ndi kuyimba; lidzapatsidwa
ulemerero wa Lebano, ndi ukuru wa Karimeli ndi Saroni; anthuwo
adzaona ulemerero wa Yehova, ukuru wace wa Mulungu wathu.
3Limbitsani manja opanda mphamvu, ndi kulimbitsa maondo a
gwedegwede. 4Nenani kwa a mitima ya cinthenthe, Limbani,
musaope; taonani, Mulungu wanu adza ndi kubwezera cilango, ndi
mphotho ya Mulungu; Iye adzafika ndi
kukupulumutsani. 5Pamenepo maso a akhungu adzatsegudwa, ndi
makutu a ogontha adzatsegulidwa. 6Pamenepo wopunduka
adzatumpha ngati nswala, ndi lilume la wosalankhula lidzayimba;
pakuti m'cipululu madzi adzaturuka, ndi mitsinje m'dziko loti
se. 7Ndipo mcenga wong'azimira udzasanduka thamanda, ndi
nthaka yopanda madzi idzasanduka zitsime zamadzi; m'malo a
ankhandwe m'mene iwo anagona, mudzakhala udzu ndi mabango
ndi milulu. 8Ndipo kudzakhala khwalala kumeneko, ndi njira, ndipo
idzachedwa njira yopatulika; audio sadzapita m'menemo; koma Iye
adzakhala nao oyenda m'njira, ngakhale opusa, sadzasocera
m'menemo. 9Sikudzakhala mkango kumeneko, ngakhale cirombo
colusa sicidzapondapo, pena kupezedwa pamenepo; koma
akuomboledwa adzayenda m'menemo, 10ndiro oomboledwa a
Yehova adzabwera, nadzafika ku Ziyoni alikuyimba; kukondwa
kosatha kudzakhala pa mitu yao; iwo adzakhala ndi kusekerera ndi
kukondwa, ndipo cisoni ndi kuusa moyo kudzacoka.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Nkhondo ya Sanakeribu idzera Yerusalemu

1Koma panali caka cakhumi ndi cinai ca mfumu Hezekiya,
Sanakeribu, mfumu ya Asuri anadza, nathira nkhondo pa midzi ya
malinga yonse ya Yuda, nailanda. 2Ndipo mfumu ya Asuri
inatumiza kazembe kucokera pa Lakisi, kunka ku Yerusalemu, kwa
mfumu Hezekiya, ndi nkhondo yambiri. Ndipo iye anaima cifupi ndi
mcerenje wa thamanda la kumtunda, m'khwalala la pa mwaniko
wa wotsuka nsaru. 3Ndipo anamturukira Eliakimu, mwana wa
Hilikiya, amene anali wapanyumba, ndi Sebina, mlembi, ndi Yoaki,
mwana wa Asafu, mkumbutsi. 4Ndipo kazembeyo anati kwa iwo,
Nenani inu tsopano kwa Hezekiya, Itero mfumu yaikuru, mfumu ya
Asuri, Kodi cikhulupiriro ici ncotani, ucikhulupirira iwe? 5Ine nditi,
Uphungu wako, ndi mphamvu zako za kunkhondo, zingokhala mau
acabe; tsopano ukhulupirira yani, kuti wandipandukira ine? 6Taona,
ukhulupirira ndodo yabango iyi yophwanyika, kunena Aigupto;
imene munthu akaitsamira, idzalowa m'dzanja mwace, ndi
kulipyoza; momwemo Farao, mfumu ya Aigupto, kwa onse amene
amkhulupirira iye. 7Koma ukanena kwa ine, Ife tikhulupirira Yehova
Mulungu wathu; kodi si ndiye amene Hezekiya wacotsa misanje
yace ndi maguwa ace a nsembe, nati kwa Yuda, ndi kwa
Yerusalemu, Inu mudzapembedzera patsogolo pa suwa la nsembe
ili? 8Cifukwa cace upereketu zikole kwa mbuyanga, mfumu ya
Asuri, ndipo ine ndidzakupatsa iwe akavalo zikwi ziwiri, ngati iwe
udzaona okwerapo. 9Bwanji tsono iwe ungathe kubweza nkhope ya
nduna mmodzi wamng'ono wa atumiki a mbuyanga, ndi
kukhulupirira Aigupto, kuti adzakupatsa magareta ndi
apakavalo? 10Ndipo ine tsopano, kodi ndafika opanda Yehova
kudzamenyana ndi dziko ili, kudzalipasula? Yehova anati kwa ine,
Kwera, ndi kumenyana ndi dziko ili, ndi kulipasula. 11Ndipo
Eliakimu, ndi Sebina, ndi Yoaki, anati kwa kazembeyo, Nenanitu
kwa atumiki anu m'cinenero ca Aramu; pakuti ife ticimva; ndipo
musanene kwa ife m'Ciyuda, m'makutu a anthu amene ali
palinga. 12Koma kazembeyo anati, Kodi mbuyanga ananditumiza
ine kwa mbuyako ndi kwa iwe kunena mau amenewa? kodi iye
sananditumiza ine kwa amuna okhala palinga, kuti adye ndowe
zao zao, ndi kumwa madzi ao ao ndi inu? 13Pamenepo kazembeyo
anaima, napfuula ndi mau akuru m'Ciyuda, nati, Imvani, inu, mau a
mfumu yaikuru, mfumu ya Asuri. 14Mfumu itere, Musaleke
Hezekiya anyenge inu; pakuti iye sadzathai
kukupulumutsani: 15ngakhale musaleke Hezekiya akhulupiritse inu
kwa Yehova, ndi kunena, Yehova adzatipulumutsa ndithu; mudzi
uwu sudzaperekedwa m'manja mwa mfumu ya Asuri. 16Musamvere

Hezekiya, pakuti mfumu ya ku Asuri itere, Mupangane nane, turukirani kwa ine; ndipo yense adye mphesa zace, ndi nkhuyu zace, namwe yense madzi a pa citsime cace; 17kufikira ine ndidzadza, ndi kunka nanu ku dziko lofanana ndi lanu, dziko la tirigu ndi vinyo, dziko la cakudya ndi minda yamphesa. 18Cenjerani angakukopeni inu Hezekiya, ndi kuti, Yehova adzatipulumutsa ife. Kodi milungu iri yonse ya amitundu inapulumutsa dziko lao m'manja mwa mfumu ya ku Asuri? 19Iri kuti milungu ya Hamati, ndi Aripadi? iri kuti milungu ya Sefaravaimu? kodi inapulumutsa Samariya m'manja mwanga? 20Mwa milungu yonse ya maiko awa, inapulumutsa dziko lao m'manja mwanga ndi iti, kuti Yehova adzapulumutsa Yerusalemu m'manja mwanga? 21Koma iwo anakhala cete, osamuyankha mau, pakuti mfumu inawalamulira kuti, Musamuyankhe. 22Ndipo anafika Eliakimu, mwana wa Hilikiya, amene anali wapanyumba, ndi Sebina, mlembi, ndi Yoaki, mwana wa Asafu, mkumbutsi, kwa Hezekiya ndi zobvala zao zong'ambika, namuuza iye mau a kazembeyo.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Mwa mantha Hezekiya aitana mnenert Yesaya

1Ndipo panali pamene mfumu Hezekiya anamva, anang'amba
zobvala zace, nabvala ciguduli, nalowa m'nyumba ya
Yehova. 2Ndipo anatumiza Eliakimu, wapanyumba, ndi Sebina,
mlembi, ndi akuru a nsembe, atapfunda ciguduli, kwa Yesaya,
mneneri, mwana wa Amozi. 3Ndipo iwo anati kwa iye, Hezekiya
atere, Tsiku lalero ndilo tsiku la bvuto, ndi lakudzudzula, ndi
citonzo; pakuti nthawi yace yakubala ana yafika, ndipo palibe
mphamvu yobalira. 4Kapena Yehova Mulungu wako adzamva mau
a kazembeyo, amene mfumu ya Asuri mbuyace inamtuma
kukatonza Mulungu wamoyo, nadzadzudzula mau amene Yehova
Mulungu wako adawamva; cifukwa cace, kweza pemphero lako
cifukwa ca otsala osiyidwa. 5Ndipo atumiki a mfumu Hezekiya
anadza kwa Yesaya. 6Ndipo Yesaya anati kwa iwo, Mukati kwa
mbuyanu, Atero Yehova, musaope mau amene wawamva iwe,
amene atumiki a mfumu ya Asuri andilalatira Ine. 7Taonani,
ndidzaika mzimu mwa iye, ndipo iye adzamva mbiri, nadzabwerera
kunka ku dziko la kwao; ndipo ndidzamgwetsa ndi lupanga m'dziko
la kwao.

Uthenga wa Sanakeribu wa kwa Hezekiya

8Ndipo kazembeyo anabwerera, napeza mfumu ya Asuri
irikuponyana nkhondo ndi Libina; pakuti anamva kuti inacoka ku
Lakisi. 9Ndipo anamva anthu alinkunena za Tiraka, mfumu ya Kusi,
Iye waturuka kudzamenyana ndi iwe. Ndipo pamene anamva, iye
anatumiza mithenga kwa Hezekiya ndi kuti, 10Mukati kwa
Hezekiya, mfumu ya Yuda, Asakunyenge Mulungu wako, amene
iwe umkhulupirira, ndi kuti, Yerusalemu sadzaperekedwa m'manja
mwa mfumu ya Asuri. 11Taona, iwe wamva cimene mafumu a Asuri
anacitira maiko onse, ndi kuwapasula konse; ndipo kodi iwe
udzapulumutsidwa? 12Kodi milungu ya amitundu yaipulumutsa iyo,
imene atate anga anaipasula? Gozani ndi Harani ndi Rezefi ndi ana
a Edeni amene anali m'Telasara. 13Iri kuti mfumu ya ku Hamati, ndi
mfumu ya ku Aripadi, ndi mfumu yamudzi wa ku Sefaravaimu, ya
ku Hena, ndi Iveva?

Pemphero la Hezekiya

14Ndipo Hezekiya analandira kalatayo m'manja mwa mithengayo,
namuwerenga; ndipo Hezekiya anakwera kunka ku nyumba ya
Yehova, namfunyulula pamaso pa Yehova. 15Ndipo Hezekiya
anapemphera kwa Yehova, nati, 16Yehova wa makamu, Mulungu
wa Israyeli, amene mukhala pa akerubi, Inu ndinu Mulungu, Inu
nokha, wa maufumu onse a dziko lapansi, Inu munalenga
kumwamba ndi dziko lapansi. 17Cherani makutu anu, Yehova,

nimumve; tsegulani maso anu, Yehova, nimuone; ndi kumva mau onse a Sanakeribu, amene watumiza kumtonza Mulungu wamoyo. 18Zoonadi, Yehova, mafumu a Asuri anaononga maiko onse, ndi pokhala pao. 19Ndipo anaponya milungu yao pamoto; pakuti iyo sinali milungu, koma nchito yopangidwa ndi manja a anthu, mtengo ndi mwala; cifukwa cace iwo anaiononga, 20Cifukwa cace, Yehova, Mulungu wathu, mutipulumutse ife m'manja mwace, kuti maufumu onse a dziko adziwe, kuti Inu ndinu Yehova, Inu nokha.

Kuyankha kwa Yehova mwa Yesaya

21Ndipo Yesaya, mwana wa Amozi, anatumiza kwa Hezekiya, ndi kuti, Atero Yehova, Mulungu wa Israyeli, Popeza wandipemphera za Sanakeribu mfumu ya Asuri, 22awa ndiwo mau amene Yehova wanena za iye, Namwali, mwana wamkazi wa Ziyoni, wakunyoza iwe ndi kuseka iwe ndi ciphwete; mwana wamkazi wa Yerusalemu wapukusa mutu wace pambuyo pako. 23Ndani amene, iwe wamtonza ndi kumlalatira? ndani amene iwe wakwezera mau ako ndi kutukulira maso ako kumwamba? ndiye Woyera wa Israyeli. 24Wamtonza Ambuye ndi atumiki ako, ndipo wati, Ndi khamu la magareta anga ine ndafika ku nsonga za mapiri, ku mbali za Lebano; ndipo ndidzagwetsapo mikungudza yaitali, ndi milombwa yosankhika; ndipo ine ndidzafika pamutu pace penipeni, ku nkhalango ya munda wace wobalitsa. 25Ine ndakumba ndi kumwa madzi, ndidzaumitsa nyanja zonse za Aigupto ndi kuphazi kwanga. 26Kodi iwe sunamve, kuti ndinacita ici kale, ndi kucikonza nthawi zakale? tsopano Ine ndacikwaniritsa, kuti iwe ukapasule midzi yamalinga, isanduke miunda. 27Cifukwa cace okhalamo analefuka, naopsedwa, nathedwa nzeru; ananga udzu wa in'munda, ndi masamba awisi, ndi udzu wa pamacindwi, ndi munda wa tirigu asanakule. 28Koma ndidziwa pokhala pansi pako, ndi kuturuka kwako, ndi kulowa kwako, ndi kundikwiyira kwako. 29Cifukwa ca kundikwiyira Ine kwako, ndi popeza kudzikweza kwako kwafika m'makutu mwanga. Ine ndidzaika mbedza yanga m'mphuno mwako, ndi capakamwa canga m'milomo yako, ndipo ndidzakubweza iwe m'njira yomwe unadzerayo. 30Ndipo ici cidzakhala cizindikilo kwa iwe: caka cino mudzadya zimene ziri zomera zokha, ndipo caka caciwiri mankhokwe ace; ndipo caka cacitatu bzalani ndi kudula ndi kulima minda yamphesa ndi kudya cipatso cace. 31Ndipo otsala amene opulumuka a nyumba ya Yuda adzaphukanso mizu pansi, nadzabala cipatso pamwamba. 32Pakuti mudzaoneka m'Yerusalemu, otsala ndi opulumuka m'Yerusalemu, otsala ndi opulumuka m'phiri la Ziyoni; cangu ca Yehova wa makamu cidzacita ici. 33Cifukwa cace atero Yehova za mfumu ya Asuri, Iye

sadzafika pa mudzi uno, ngakhale kuponyapo mubvi, ngakhale kufika patsogolo pace ndi cikopa, ngakhale kuunjikirapo mulu. 34Pa njira yomwe anadzerayo, abwerera yomweyo, ndipo sadzafika pa mudzi uno, ati Yehova. 35Pakuti ndidzacinjiriza mudzi uno, kuupulumutsa, cifukwa ca Ine mwini, ndi mtumiki wanga Davide. 36Ndipo mthenga wa Yehova anaturuka, naphaipha m'zitando za Asuri, zikwi zana ndi makumi asanu ndi atatu ndi zisanu, ndipo pamene anthu anauka mamawa, taonani, onse ndiwo mitembo. 37Ndipo Sanakeribu, mfumu ya Asuri, anacoka, namuka, nabwerera, nakhala pa Nineve, 38Ndipo panali, pamene iye analikupembedzera m'nyumba ya Nisiroki, mulungu wace, Adrameleki ndi Sarezeri, ana ace anampha iye ndi lupanga; ndipo iwo anapulumuka, nathawira ku dziko la ku Ararati. Ndipo Esaradoni, mwana wace, analamulira m'malo mwace.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Kudwala kwa Hezekiya ndi kuciritsidwa kwace

1Masiku amenewo Hezekiya anadwala, nafuna kufa. Ndipo Yesaya
mneneri, mwana wa Amozi, anadza kwa iye, nati kwa iye, Atero
Yehova, Konza nyumba yako, pakuti iwe udzafa, sudzakhala ndi
moyo. 2Ndipo Hezekiya analoza nkhope yace kukhoma,
napemphera kwa Yehova, nati, 3Kumbukiranitu tsopano, Yehova,
kuti ndayenda pamaso panu m'zoonadi ndi mtima wangwiro, ndipo
ndacita zabwino pamaso panu. Ndipo Hezekiya analira
kolimba. 4Ndipo anafika mau a Yehova kwa Yesaya, ndi
kuti, 5Ukanene kwa Hezekiya, Atero Yehova, Mulungu wa Davide,
kholo lako, Ndamva kupemphera kwako, ndaona misozi yako;
taona, ndidzaonjezera pa masiku ako zaka khumi ndi
zisanu. 6Ndipo ndidzakupulumutsa iwe ndi mudzi uno m'manja
mwa mfumu ya Asuri, ndipo ndidzacinjiriza mudzi uno. 7Ndipo ici
cidzakhala cizindikilo kwa iwe cocokera kwa Yehova, kuti Yehova
adzacita ici wanenaci; 8taona, ndidzabweza mthunzi wa
pamakwerero, umene watsika pa makwerero a Ahazi ndi dzuwa,
ubwerere makwerero khumi. Ndipo dzuwa linabwerera makwerero
khumi pamakwerero, pamene udatsika mthunziwo.
9Malemba a Hezekiya mfumu ya Ayuda muja anadwala, atacira
nthenda yace.
10Ine ndinati, Pakati pa masiku anga ndidzalowa m'zipata za kunsi
kwa manda; Ndazimidwa zaka zanga zotsala.
11Ndinati, Sindidzaona Yehova m'dziko la amoyo; sindidzaonanso
munthu pamodzi ndi okhala kunja kuno;
12Pokhala panga pacotsedwa, pandisunthikira monga hema
wambusa;
Ndapindapinda moyo wanga ngati muomba;
Iye adzandidula ine poomberapo;
Kuyambira usana kufikira usiku mudzanditsiriza ine.
13Ndinadzitonthoza kufikira mamawa; monga mkango, momwemo
Iye anatyolatyola mafupa anga onse;
Kuyambira usana kufikira usiku mudzanditsiriza ine.
14Ndinalankhula-lankhula ngati namzeze, pena cumba;
Ndinalira maliro ngati nkhunda;
Maso anga analephera pogadamira kumwamba.
Yehova ndasautsidwa, mundiperekere cikoli.
15Kodi ndidzanena ciani?
Iye wanena kwa ine, ndiponso Iye mwini wacita ici;
Ine ndidzayenda cete zaka zanga zonse,
Cifukwa ca zowawa za moyo wanga.
16Ambuye ndi zinthu izi anthu akhala ndi moyo.

Ndipo m'menemo monse muli moyo wa mzimu wanga;
Cifukwa cace mundiciritse ine,
Ndi kundikhalitsa ndi moyo.
17Taonani, ndinali ndi zowawa zazikuru,
Cifukwa ca mtendere wanga;
Koma Inu mokonda moyo wanga,
Munaupulumutsa m'dzanja la cibvundi,
Pakuti mwaponya m'mbuyo mwanu macimo anga onse.
18Pakuti kunsi kwa manda sikungakuyamikeni Inu;
Imfa singakulemekezeni;
Otsikira kudzenje sangaziyembekeze zoona zanu.
19Wamoyo, wamoyo, iye adzakuyamikani inu, monga ine lero;
Atate adzadziwitsa ana ace zoona zanu.
20Yehova ndiye wondipulumutsa ine;
Cifukwa cace tidzayimba nyimbo zanga, ndi zoyimba zazingwe
Masiku onse a moyo wathu m'nyumba ya Yehova.
21Ndipo Yesaya adati, Atenge mbulu wankhuyu, auike papfundo,
Ndipo iye adzacira. 22Hezekiya anatinso, Cizindikilo nciani, kuti
ndidzakwera kunka ku nyumba ya Yehova?

©The Bible Society of Malawi, 1992

Hezekiya aonetsa amithenga a ku Babulo cuma cace, Yesaya namdzudzula

1Nthawi imeneyo Merodakibaladani, mwana wa Baladani, mfumu
ya ku Babulo, anatumiza akalata ndi mphatso kwa Hezekiya;
pakuti anamva kuti iye anadwala, nacira. 2Ndipo Hezekiya
anakondwera nao, nawaonetsa nyumba yace ya cuma, siliva, ndi
golidi, ndi zonunkhira, ndi mafuta okometsetsa, ndi nyumba yonse
ya zida zace, ndi zonse zopezedwa m'zosungira zace; munalibe
kanthu m'nyumba mwace, kapena m'dziko lace lonse, kamene
Hezekiya sanawaonetsa. 3Ndipo anadza Yesaya mneneri kwa
mfumu Hezekiya, nati kwa iye, Kodi anthu awa ananena bwanji,
ndipo iwo acokera kuti, kudza kwa inu? Ndipo Hezekiya anati, Iwo
acokera ku dziko lakutari, kudza kwa ine, kunena ku Babulo. 4Ndipo
iye anati, Kodi iwo anaona ciani m'nyumba mwanu? Ndipo
Hezekiya anayankha, Zonse za m'nyumba mwanga iwo anaziona;
palibe kanthu ka mwa cuma canga, kamene ine
sindinawaonetse. 5Ndipo Yesaya anati kwa Hezekiya, Imvani mau a
Yehova wa makamu. 6Taona, masiku afika, kuti zonse za m'nyumba
mwako, ndi zimene atate ako anazikundika kufikira lero lino,
zidzatengedwa kunka ku Babulo; sipadzatsala kanthu, ati
Yehova. 7Ndipo ana ako amene adzabadwa ndi iwe, amene
udzabala, iwo adzawatenga, ndipo adzakhala adindo m'cinyumba
cace ca mfumu ya ku Babulo. 8Ndipo Hezekiya anati kwa Yesaya,
Mau a Yehova, amene iwe wanena, ali abwino. Iye anatinso, Pakuti
padzakhala mtendere ndi zoonadi masiku anga.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Lonjezo la cipulumutso ca Israyeli

1Mutonthoze, mutonthoze mtima wa anthu anga, ati Mulungu
wanu. 2Munene inu zotonthoza mtima kwa Yerusalemu,
nimupfuulire kwa iye, kuti nkhondo yace yatha, kuti kuipa kwace
kwakhululukidwa; kuti iye walandira mowirikiza m'dzanja la
Yehova, cifukwa ca macimo ace onse.
3Mau a wopfuula m'cipululu, Konzani njira ya Yehova, lungamitsani
m'dziko loti se khwalala la Mulungu wathu. 4Cigwa ciri conse
cidzadzazidwa, ndipo phiri liri lonse ndi citunda ciri conse
zidzacepetsedwa, ndipo zokhota zidzaongoledwa, ndipo
zamakolokoto zidzasalala; 5ndipo ulemerero wa Yehova
udzabvumbulutsidwa, ndipo anthu onse adzauona pamodzi, pakuti
pakamwa pa Yehova panena comweco, 6Mau a wina ati, Pfuula.
Ndipo ndinati, Kodi ndipfuule ciani? Anthu onse ndi udzu, ndi
kukoma kwao konse kunga duwa la m'thengo; 7udzu unyala, duwa
lifota; cifukwa mpweya wa Yehova waombapo; zoonadi anthu ndi
udzu. 8Udzu unyala, duwa lifota, koma mau a Mulungu wathu
adzakhala nthawi zacikhalire.
9Iwe amene utengera mau abwino ku Ziyoni, kwera iwe
pamwamba pa phiri lalitari; iwe amene utengera mau abwino ku
Yerusalemu, kweza mau ako ndi mphamvu, kwezetsa usaope, nena
ku midzi ya Yuda, Taonani, Mulungu wanu! 10Taonani, Ambuye
Yehova adzadza ngati wamphamvu, ndipo mkono wace
udzalamulira; taonani, mphoto yace iri ndi Iye, ndipo cobwezera
cace ciri patsogolo pa Iye. 11Iye adzadyetsa zoweta zace ngati
mbusa, nadzasonkhanitsa ana a nkhosa pacapa pace,
nadzawatengera pa cifuwa cace, ndipo adzatsogolera bwino bwino
zimene ziyamwitsa.

Mulungu ndi wamphamvuyonse, mafano ndi acabe

12Ndani wayesa madzi m'dzanja lace, nayesa thambo ndi cikhato,
ndi kudzaza pfumbi la nthaka m'nsengwa, ndi kuyesa mapiri
m'mbale zoyesera, ndi zitunda m'mulingo? 13Ndani anapangira
mzimu wa Yehova, kapena kukhala phungu lace, ndi kumphunzitsa
Iye? 14Iye anakhala upo ndi yani, ndipo ndani analangiza Iye ndi
kumphunzitsa m'njira ya ciweruzo, ndi kumphunzitsa nzeru ndi
kumuonetsa njira ya luntha? 15Taonani, amitundu akunga dontho la
m'mtsuko, nawerengedwa ngati pfumbi losalala la m'muyeso;
taonani atukula zisumbu ngati kanthu kakang'ono. 16Ndipo Lebano
sakwanira kutentha, ngakhale nyama zace sizikwanira nsembe
yopsereza. 17Amitundu onse ali cabe pamaso pa Iye; awayesa
ngati cinthu cacabe, ndi copanda pace, 18Mudzafanizira Mulungu
ndi yani tsopano, kapena kumyerekeza ndi cithunzithunzi

cotani? 19Pano losema mmisiri analisungunula, ndipo wosula golidi
analikuta ndi golidi, naliyengera maunyolo asiliva. 20Wosowa
nsembe yoteroyo asankha mtengo umene sungabvunde, iye
adzisankhira yekha munthu mmisiri waluso, akonze fano losema,
limene silisunthika. 21Kodi inu simunadziwe? kodi inu simunamve?
kodi sanakuuzani inu ciyambire? kodi inu simunadziwitse ciyambire
mayambiro a dziko lapansi? 22Ndi Iye amene akhala pamwamba pa
malekerezo a dziko lapansi, ndipo okhalamo akunga ziwala; amene
afutukula thambo ngati cinsaru, naliyala monga hema
wakukhalamo; 23amene asandutsa akalonga kuti akhale acabe,
nasandutsa oweruza a dziko lapansi akhale opanda pace, 24Inde
sanaokedwe, inde sanafesedwe; inde, muzu wao sunazike pansi;
koma Iye anawaombetsera mphepo, ndipo afota, ndipo
kabvumvulu awacotsa monga ciputu. 25Mudzandifanizira Ine ndi
yani tsono, kuti ndilingane naye, ati Woyerayo. 26Kwezani maso
anu kumwamba, muone amene analenga izo, amene aturutsa
khamu lao ndi kuziwerenga; azicha zonse maina ao, ndi mphamvu
zace zazikuru, ndi popeza ali wolimba mphamvu, palibe imodzi
isoweka.
27Bwanji iwe, Yakobo, umati, ndi bwanji umanena iwe, Israyeli,
Njira yanga yabisika kwa Yehova; ndipo ciweruzo ca Mulungu
wanga candipitirira? 28Kodi iwe sunadziwe? kodi sunamve?
Mulungu wacikhalire, Yehova, Mlengi wa malekezero a dziko
lapansi, salefuka konse, salema; nzeru zace sizisanthulika. 29Iye
alimbitsa olefuka, naonjezera mphamvu iye amene alibe
mphamvu. 30Ngakhale anyamata adzalefuka ndi kulema ndi
amisinkhu adzagwa ndithu: 31koma iwo amene alindira Yehova
adzatenganso mphamvu; adzauluka pamwamba ndi mapiko
monga ziombankhanga; adzathamanga kuma osalema; adzayenda
koma osalefuka.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Yesaya 41

Yehova yekha ndiye Mulungu, Israyeli amkhulupirire Iye yekha yekha

1Khalani cete pamaso pa Ine, zisumbu inu, anthu atengenso
mphamvu; ayandikire; pamenepo alankhule; tiyeni, tiyandikire
pamodzi kuciweruziro. 2Ndani anautsa wina wocokera kum'mawa,
amene amuitana m'cilungamo, afike pa phazi lace? Iye apereka
amitundu patsogolo pace, namlamuliritsa mafumu; nawapereka
monga pfumbi ku lupanga lace, monga ciputu couluzidwa ku uta
wace. 3Iye awathamangitsa, napitirira mwamtendere; pa njira
imene asanapitemo ndi mapazi ace. 4Ndani wacipanga, nacimariza
ico, kuchula mibadwo ciyambire? Ine Yehova, ndine woyamba, ndi
pacimariziro ndine ndemwe. 5Zisumbu zinaona niziopa;
malekezero a dziko lapansi ananthunthumira; anayandikira,
nafika. 6Iwo anathangata yense mnansi wace, ndi yense anati kwa
mbale wace, Khala wolimba mtima. 7Cotero mmisiri wa mitengo
analimbikitsa wosula golidi, ndi iye amene asalaza ndi nyundo
anamlimbikitsa iye amene amenya posulira, nanena za kulumikiza
ndi nthobvu, Kuti kwabwino; ndipo iye akhomera fanolo misomali
kuti lisasunthike.
8Koma iwe, Israyeli, mtumiki wanga, Yakobo, amene
ndinakusankha, mbeu ya Abrahamu bwenzi langa; 9iwe amene
ndinakuwira iwe zolimba kucokera ku malekezero a dziko lapansi,
ndi kukuitana iwe kucokera m'ngondya zace, ndipo ndinati kwa
iwe, Ndiwe mtumiki wanga ndakusankha, sindinakutaya
kunja; 10usaope, pakuti Ine ndiri pamodzi ndi iwe; usaopsyedwe,
pakuti Ine ndine Mulungu wako; ndidzakulimbitsa; inde,
ndidzakuthangata; inde, ndidzakucirikiza ndi dzanja langa lamanja
la cilungamo. 11Taona, onse amene akukwiyira iwe adzakhala ndi
manyazi, nasokonezedwa; iwo amene akangana ndi iwe adzakhala
ngati cabe, nadzaonongeka. 12Iwe udzawafuna osawapeza,
ngakhale iwo amene akangana ndi iwe; ocita nkhondo ndi iwe,
adzakhala ngati cabe, ndi monga kanthu kopanda pace. 13Pakuti
Ine Yehova Mulungu wako ndidzagwira dzanja lako lamanja, ndi
kunena kwa iwe, Usaope ndidzakuthandiza iwe. 14Usaope, Yakobo,
nyongolotsi iwe, ndi anthu inu a Israyeli; ndidzakuthangata iwe, ati
Yehova, ndiye Mombolo wako, Woyera wa Israyeli. 15Taona,
ndidzakuyesa iwe coombera tirigu catsopano cakuthwa cokhala ndi
mano; iwe udzaomba mapiri ndi kuwapera asalale, ndi kusandutsa
zitunda mungu. 16Iwe udzawakupa, ndi mphepo idzawauluza;
ndipo kabvumvulu adzawamwaza; ndipo iwe udzasangalala mwa
Yehova, udzadzikuza mwa Woyera wa Israyeli, 17Wosauka ndi

wosowa afuna madzi, ndipo palibe, ndi lilume lao lilephera, cifukwa
ca ludzu; Ine Yehova ndidzawayankha, Ine Mulungu wa Israyeli
sindidzawasiya. 18Ndidzagwetsa mitsinje pazitunda zoti se, ndi
akasupe pakati pa zigwa; ndidzasandutsa cipululu, cikhale
thamanda lamadzi, ndi mtunda wouma ukhale magwero a
madzi. 19Ndidzabzala m'cipululu mkungudza, ndi msangu, ndi
mcisu, ndi mtengo waazitona; ndidzaika m'cipululu pamodzi
mlombwa, ndi mkuyu, ndi naphini; 20kuti iwo aone ndi kudziwa, ndi
kulingalira, ndi kumvetsa pamodzi, kuti dzanja la Yehova lacita ici,
ndipo Woyera wa Israyeli wacilenga ici.
21Onetsani mlandu wanu, ati Yehova; turutsani zifukwa zanu
zolimba, ati Mfumu ya Yakobo. 22Aziturutse, atichulire ife, cimene
cidzaoneka; chulani inu zinthu zakale, zinali zotani, kuti ife
tiganizire pamenepo, ndi kudziwa mamariziro ao; kapena
tionetseni ife zinthu zimene zirinkudza. 23Chulani zinthu zimene
zirinkudza m'tsogolo, kuti ife tidziwe kuti inu ndinu milungu; inde,
citani zabwino, kapena citani zoipa, kuti ife tiopsyedwe, ndi kuona
pamodzi. 24Taonani, inu muli acabe, ndi nchito yanu yacabe;
wonyansa ali iye amene asankha inu.
25Ndautsa wina wakucokera kumpoto; ndipo iye wafika wakucokera
poturuka dzuwa, amene achula dzina langa; ndipo iye adzafika pa
olamulira, monga matope, ndi monga muumbi aponda dothi la
mbiya. 26Ndani wachula ico ciyambire, kuti ife ticidziwe? ndi nthawi
zakale, kuti ife tinene, Iye ali wolungama? inde, palibe wina amene
achula, inde, palibe wina amene asonyeza, inde, palibe wina
amene amvetsa mau anu. 27Poyamba Ine ndidzati kwa Ziyoni,
Taona, taona iwo; ndipo ndidzapereka kwa Yerusalemu wina,
amene adza ndi mau abwino. 28Ndipo pamene ndayang'ana, palibe
munthu; ngakhale mwa iwo, palibe phungu, amene angathe
kuyankha mau, pamene ndiwafunsa. 29Taona, iwo onse, nchito zao
zikhala zopanda pace ndi zacabe; mafano ao osungunula ndiwo
mphepo ndi masokonezo.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Mtumiki wa Yehova

1Taona Mtumiki wanga, amene ndimgwiriziza; Wosankhika wanga,
amene moyo wanga ukondwera naye; ndaika mzimu wanga pa Iye;
Iye adzaturutsira amitundu ciweruziro. 2Iye sadzapfuula, ngakhale
kukuwa, pena kumvetsa mau ace m'khwalala. 3Bango lophwanyika
sadzalityola, ndi lawi lozirala sadzalizima; adzaturutsa ciweruzo
m'zoona. 4Iye sadzalephera kapena kudololoka, kufikira
atakhazikitsa ciweruzo m'dziko lapansi; ndipo zisumbu zidzalindira
cilamulo cace. 5Atero Mulungu Yehova, Iye amene analenga
thambo, nalifutukula, nayala ponse dziko lapansi, ndi cimene
cituruka m'menemo, Iye amene amapatsa anthu a m'menemo
mpweya, ndi mzimu kwa iwo amene ayenda m'menemo; 6Ine
Yehova ndakuitana Iwe m'cilungamo, ndipo ndidzagwira dzanja
lako ndi kusunga Iwe, ndi kupatsa Iwe ukhale pangano la anthu,
ndi kuunika kwa amitundu; 7kuti utsegule maso akhungu, uturutse
am'nsinga m'ndende, ndi iwo amene akhala mumdima, aturuke
m'nyumba ya kaidi. 8Ine ndine Yehova; dzina langa ndi lomweli;
ndipo ulemerero wanga Ine sindidzapereka kwa wina, ngakhale
kunditamanda kwa mafano osemedwa. 9Taona, zinthu zakale
zaoneka, ndipo zatsopano Ine ndizichula; zisanabuke
ndidzakumvetsani.
10Yimbirani Yehova nyimbo yatsopano, ndi matamando ace
kucokera ku malekezero a dziko lapansi; inu amene mutsikira
kunyanja, ndi zonse ziri m'menemo, zisumbu ndi okhala
mommo. 11Cipululu ndi midzi yace ikweze mau ao, midzi imene
Kedara akhalamo; okhala m'Sela ayimbe, akuwe kucokera
pamwamba pa mapiri. 12Apereke ulemerero kwa Yehova, anene
matamando ace m'zisumbu. 13Yehova adzaturuka ngati munthu
wamphamvu; adzautsa nsanje ngati munthu wa nkhondo; Iye
adzapfuula, inde adzakuwa zolimba; adzacita zamphamvu pa
adani ace. 14Ndakhala nthawi yambiri wosalankhula; ndakhala cete
ndi kudzithungata ndekha; tsopano ndidzapfuula ngati mkazi
wobala; ndidzapuma modukizadukiza ndi wefuwefu
pamodzi. 15Ndidzapasula mapiri ndi zitunda, ndi kuumitsa
zitsamba zao zonse; ndi kusandutsa nyanja zisumbu, ndi kuumitsa
matamanda. 16Ndipo ndidzayendetsa akhungu m'khwalala, limene
iwo salidziwa; m'njira zimene iwo sazidziwa ndidzawatsogolera;
ndidzawalitsa mdima m'tsogolo mwao, ndi kulungamitsa malo
okhota. Zinthu Izi ine ndidzacita, ndipo sindidzawasiya. 17Iwo
adzabwezedwa m'mbuyo, adzakhala ndi manyazi ambiri amene
akhulupirira mafano osemedwa, nati kwa mafano oyengeka, Inu
ndinu milungu yathu.

18Imvani, agonthi inu; yang'anani, akhungu inu, kuti
muone. 19Ndani ali wakhungu, koma mtumiki wanga? pena
wagonthi, monga mthenga wanga, amene ndimtumiza? ndani ali
wakhungu monga bwenzi langa, ndi wakhungu monga mtumiki wa
Yehova? 20Iwe waona zinthu zambiri, koma susamalira konse;
makutu ako ali otseguka, koma sumva konse. 21Cinakondweretsa
Yehova cifukwa ca cilungamo cace kukuza cilamulo, ndi
kucilemekeza. 22Koma awa ndiwo anthu olandidwa zao ndi
kufunkhidwa; iwo onse agwa m'mauna, nabisidwa m'nyumba
zakaidi; alandidwa zao, palibe wowapulumutsa; afunkhidwa ndipo
palibe woti, Bwezerani. 23Ndani mwa inu adzachera khutu lace
pamenepo? amene adzamvera ndi kumva nthawi
yakudza? 24Ndani anapereka Yakobo, kuti afunkhidwe, ndi Israyeli,
kuti awawanyidwe? kodi si Yehova? Iye amene tamcimwira, ndi
amene iwo anakonda kuyenda m'njira zace, ngakhale kumvera
ciphunzitso cace. 25Cifukwa cace anatsanulira pa iye mkwiyo wace
waukali, ndi mphamvu za nkhondo; ndipo unamyatsira moto
kuzungulira kwace, koma iye sanadziwa; ndipo unamtentha, koma
iye sanacisunga m'mtima.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Mulungu Yehova yekha apulumutsa Israyeli

1Koma tsopano atero Yehova, amene anakulenga iwe Yakobo, ndi
Iye amene anakupanga iwe Israyeli, Usaope, cifukwa ndakuombola
iwe, ndakuchula dzina lako, iwe uli wanga. 2Pamene udulitsa
pamadzi ndiri pamodzi ndi iwe; ndi pooloka mitsinje
sidzakukokolola; pakupyola pamoto sudzapsya; ngakhale lawi
silidzakutentha. 3Cifukwa kuti Ine ndine Yehova Mulungu wako,
Woyera wa Israyeli, Mpulumutsi wako; ndapatsa Aigupto dombolo
lako, Etiopia ndi Seba m'malo mwako. 4Pokhala iwe wa mtengo
wapatari pamaso panga, ndi wolemekezeka, ndipo ndakukonda
iwe; Ine ndidzakuombola ndi anthu, ndi kupereka anthu m'malo
mwa moyo wako. 5Usaope; pakuti Ine ndiri ndi iwe; ndidzatenga
mbeu zako kucokera kum'mawa, ndi kusonkhanitsa iwe kucokera
kumadzulo. 6Ine ndidzati ndi kumpoto, Pereka; ndi kumwera,
Usaletse; bwera nao ana anga amuna kucokera kutari, ndi ana
anga akazi kucokera ku malekezero a dziko lapansi; 7yense
wochedwa dzina langa, amene ndinamlenga cifukwa ca ulemerero
wanga; ndinamuumba iye; inde, ndinampanga iye. 8Turutsani
anthu akhungu, amene ali ndi maso, ndi agonthi, amene ali ndi
makutu. 9Amitundu onse asonkhane pamodzi, ndi anthu aunjikane;
ndani mwa iwo anganene ici ndi kuonetsa ife zinthu zakale? atenge
mboni zao, kuti abvomerezeke ndi olungama; pena amve, nanene
zoonadi. 10Inu ndinu mboni zanga, ati Yehova, ndi mtumiki wanga,
amene ndakusankha; kuti mundidziwe, ndi kundikhulupirira Ine,
ndi kuzindikira, kuti Ine ndine; ndisanakhale Ine, panalibe Mulungu
wolengedwa, ngakhale pambuyo panga sipadzakhala wina. 11Ine,
Inetu ndine Yehova; ndipo palibe Mpulumutsi, koma Ine
ndekha. 12Ine ndalalikira, ndipo ndikupulumutsa ndi kumvetsa,
ndipo panalibe Mulungu wacilendo pakati pa inu; cifukwa cace inu
ndinu mboni zanga, ati Yehova, ndipo Ine ndine Mulungu. 13Inde
ciyambire nthawi Ine ndine, ndipo palibe wina wopulumutsa
m'dzanja langa; ndidzagwira nchito, ndipo ndani adzaletsa?
14Atero Yehova, Mombolo wanu, Woyera wa Israyeli: Cifukwa ca inu
ndatumiza ku Babulo, ndipo ndidzatsitsira iwo onse monga othawa,
ngakhale Akasidi m'ngalawa za kukondwa kwao. 15Ine ndine
Yehova Woyera wanu, Mlengi wa Israyeli, Mfumu yanu, 16Atero
Yehova, amene akonza njira panyanja, ndi popita m'madzi
amphamvu; 17amene aturutsa gareta ndi ka valo, nkhondo ndi
mphamvu; iwo agona pansi pamodzi sadzaukai; iwo atha,
azimidwa ngati lawi. 18Musakumbukire zidapitazo, ngakhale
kulingalira zinthu zakale. 19Taonani, ine ndidzacita cinthu
catsopano; tsopano cidzaoneka; kodi simudzacidziwa?

Ndidzakonzadi njira m'cipululu, ndi mitsinje m'zidalala. 20Nyama za
m'thengo zidzandilemekeza, ankhandwe ndi nthiwatiwa; cifukwa
ndipatsa madzi m'cipululu, ndi mitsinje m'mkhwangwala,
ndimwetse anthu anga osankhika; 21anthu amene ndinadzilengera
ndekha, kuti aonetse matamando anga. 22Komabe iwe
sunandiitane Ine, Yakobo; koma iwe walema ndi Ine, Israyeli. 23Iwe
sunanditengere Ine zoweta zazing'ono za nsembe zopsereza zako;
kapena kundilemekeza ndi nsembe zako. Sindinakutumikiritsa ndi
nsembe zaufa, kapena kukutopetsa ndi zonunkhira. 24Iwe
sunandigulire Ine nzimbe ndi ndarama, pena kundikhutitsa ndi
mafuta a nsembe zako. Koma iwe wanditumikiritsa ndi macimo
ako, wanditopetsa ndi mphulupulu zako. 25Ine, Inedi, ndine amene
ndifafaniza zolakwa zako, cifukwa ca Ine mwini; ndipo Ine
sindidzakumbukira macimo ako. 26Undikumbutse Ine; tiyeni,
tinenane pamodzi; fotokoza mlandu wako, kuti
ukalungamitsidwe. 27Atate wako woyamba anacimwa, ndi
otanthauzira ako andilakwira Ine. 28Cifukwa cace ndidzaipitsa
akuru a kacisi, ndipo ndidzasanduliza Yakobo akhale temberero, ndi
Israyeli akhale citonzo.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Mulungu ndi wamkulukulu, mafano ndi acabe

1Koma tsopano, imva Yakobo, mtumiki wanga, ndi Israyeli, amene
ndakusankha; 2atero Yehova, amene anakutenga iwe, nakuumba
kucokera m'mimba, amene adzathangata iwe. Usaope Yakobo,
mtumiki wanga ndi iwe, Yesuruni, amene ndakusankha iwe. 3Pakuti
ndidzathira madzi pa dziko limene liribe madzi, ndi mitsinje pa
nthaka youma; ndidzathira mzimu wanga pa mbeu yako, ndi
mdalitso wanga pa obadwa ako; 4ndipo iwo adzaphuka pakati pa
maudzu, ngati msondodzi m'mphepete mwa madzi. 5Wina adzati,
Ine ndiri wa Yehova; ndi wina adzadzicha yekha ndi dzina la
Yakobo, ndipo wina adzalemba ndi dzanja lace, Ndine wa Yehova,
ndi kudzicha yekha ndi mfunda wa Israyeli.
6Atero Yehova, Mfumu ya Israyeli ndi Mombolo wace, Yehova wa
makamu, Ine ndiri woyamba ndi womariza, ndi popanda Ine
palibenso Mulungu. 7Ndipo ndani adzaitana monga Ine, ndi
kulalikira ici ndi kundilongosolera ici, cikhazikitsire Ine anthu akale?
milunguyo iwadziwitse zomwe zirinkudza, ndi za
m'tsogolo. 8Musaope inu, musakhale ndi mantha; kodi ndinanena
kwa iwe zakale, ndi kuzionetsa zimenezo, ndipo inu ndinu mboni
zanga. Kodi popanda Ine aliponso Mulungu? Iai, palibe thanthwe;
sindidziwa liri lonse. 9Omwe apanga fano losema onsewo
asokonezeka; ndipo zokondweretsa zao sadzapindula nazo kanthu;
ndipo mboni zao siziona, kapena kudziwa; kuti akhale ndi
manyazi. 10Ndani wapanga mulungu, kapena kusungunula fano
losema losapindula kanthu? 11Taonani anzace onse adzakhala ndi
manyazi, ndi amisiri ace ndi anthu; asonkhane onse pamodzi,
aimirire; adzaopa, iwo onse adzakhala ndi manyazi. 12Wacipala
acita zace ndi nsompho, nagwira nchito ndi makala, nafanizira
fanolo ndi nyundo, nagwira nchito yace ndi mkono wace
wamphamvu; inde, ali ndi njala, ndipo mphamvu zace zilephera;
iye samwa madzi, nalefuka. 13Mmisiri wa mitengo atambalitsa
cingwe; nalilemba ndi colembera, nalikonza ndi ncerero, nalilemba
ndi zolinganizira, nalifanizira monga maonekedwe a munthu,
monga munthu wokongola, kuti likhale m'nyumba. 14Iye adzidulira
yekha mikungudza, natenga mtengo wambawa, ndi wathundu, ndi
kudzisankhira yekha wina wa mitengo ya nkhalango; naoka
mtengo wamlombwa, mvula niukulitsa. 15Ndipo udzakhala kuti
munthu autenthe; iye natengako, nauotha moto; inde auyatsa,
naoca mkate; inde, apanga mlungu, naulambira, naupanga fano
losema, naligwadira. 16Iye atenthako mbali yina pamoto; ndi mbali
yinayo adya nyama; akazinga zokazinga, nakhuta, inde, aotha
moto, nati, Ha, ndakongonoka, ndauona moto. 17Ndipo cotsalaco

apanga mlungu, ngakhale fano lace losema; iye aligwadira,
nalipembedza, nalipemphera nati, Ndipulumutse ine, cifukwa kuti
ndinu mulungu wanga. 18Iwo sadziwa, kapena kuzindikira, cifukwa
pamaso pao papakidwa thope, kuti sangaone, ndi m'mitima mwao
kuti sangadziwitse. 19Palibe wina wokumbukira, kapena kudziwa,
kapena kuzindikira, ndi kuti, Ndatentha mbali yina pamoto, inde
ndaocanso mkate pamakala pace, ndakazinga nyama ndi kuidya;
kodi ndicipange cotsala cace, cikhale conyansa? ndidzagwadira
kodi tsinde la mtengo? 20Iye adya phulusa; mtima wodzinyenga
wampambutsa, kuti iye sangapulumutse moyo wace, pena kunena,
Kodi simuli kunama m'dzanja langa lamanja?

Mulungu Mpulumutsi wa Israyeli

21Kumbukira zinthu izi, Yakobo; ndi Israyeli, pakuti iwe ndiwe
mtumiki wanga; ndakuumba, iwe ndiwe mtumiki wanga, Israyeli,
sindidzakuiwala. 22Ine ndafafaniza monga mtambo wocindikira
zolakwa zako, ndi monga mtambo macimo ako; bwerera kwa Ine,
pakuti ndakuombola. 23Yimbani m'mwamba inu, pakuti Yehova
wacicita ico; kuwani inu, mbali za pansi pa dziko; yimbani mapiri
inu; nkhalango iwe, ndi mitengo yonse m'menemo; cifukwa kuti
Yehova wapulumutsa Yakobo, ndipo adzadzilemekezetsa yekha
mwa Israyeli.
24Atero Yehova, Mombolo wako, ndi Iye amene anakuumba iwe
m'mimba, Ine ndine Yehova, amene ndipanga zinthu zonse, ndi
kufunyulula ndekha zakumwamba, ndi kuyala dziko lopansi; ndani
ali ndi Ine? 25Ndine amene nditsutsa zizindikilo za matukutuku, ndi
kucititsa misala oombeza ula; ndi kubwezera m'mbuyo anthu
anzeru, ndi kupusitsa nzeru zao: 26Ndine amene ndilimbitsa mau a
mtumiki wanga, kucita uphungu wa amithenga anga; ndi kunena
za Yerusalemu, Adzakhalamo anthu; ndi za midzi ya Yuda;
Idzamangidwa; ndipo ndidzautsa malo abwinja ace. 27Ndine amene
nditi kwa nyanja yakuya, Iphwa, ndipo ndidzaumitsa nyanja
zako; 28ndi kunena za Koresi, Iye ndiye mbusa wanga, ndipo
adzacita zofuna zanga zonse; ndi kunena za Yerusalemu,
Adzamangidwa; ndi kwa Kacisi, Maziko ako adzaikidwa.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Yehova amuyesa Koresi cipangizo cace

1Atero Yehova kwa wodzozedwa wace kwa Koresi, amene dzanja
lace lamanja ndaligwiritsa, kuti agonjetse mitundu ya anthu
pamaso pace, ndipo ndidzamasula m'cuuno mwa mafumu;
atsegule zitseko pamaso pace, ndi zipata
sizidzatsekedwa: 2Ndidzakutsogolera ndi kusalaza pokakala;
ndidzatyolatyola zitseko zamkuwa, ndi kudula pakati akapici
acitsulo; 3ndipo ndidzakupatsa iwe cuma ca mumdima, ndi
zolemera zobisika za m'malo am'tseri, kuti iwe udziwe kuti Ine
ndine Yehova, amene ndikuitana iwe dzina lako, ndine Mulungu wa
Israyeli. 4Ndakuitana iwe dzina lako, cifukwa ca Yakobo mtumiki
wanga ndi Israyeli wosankhidwa wanga; ndakuonjezera dzina,
ngakhale iwe sunandidziwa Ine. 5Ine ndiri Yehova, ndipo palibe
winanso; popanda Ine palibe Mulungu; ndidzakumanga m'cuuno,
ngakhale sunandidziwa; 6kuti anthu akadziwe kucokera ku
maturukiro a dzuwa ndi kumadzulo, kuti palibe wina popanda Ine;
Ine ndine Yehova, palibe winanso. 7Ine ndilenga kuyera ndi mdima,
Ine ndilenga mtendere ndi coipa, Ine ndine Yehova wocita zinthu
zonse zimenezi.
8Igwani pansi, inu m'mwamba, kucokera kumwamba, thambo
litsanulire pansi cilungamo; dziko lapansi litseguke, kuti libalitse
cipulumutso, nilimeretse cilungamo cimere pamodzi; Ine Yehova
ndinacilenga cimeneco.
9Tsoka kwa iye amene akangana ndi Mlengi wace! phale mwa
mapale a dziko lapansi! Kodi dongo linganene kwa iye amene
aliumba, Kodi upanga ciani? pena nchito yako, Iye alibe
manja? 10Tsoka kwa iye amene ati kwa atate wace, Kodi iwe
ubalanji? pena kwa mkazi, Ulikusauka ninji iwe? 11Atero Yehova
Woyera wa Israyeli ndi Mlengi wace, Ndifunse Ine za zinthu zimene
zirinkudza; za ana anga amuna, ndi za nchito ya manja anga,
ndilamulireni Ine. 12Ine ndalenga dziko lapansi, ndalengamo
munthu; Ine, ngakhale manja anga, ndafunyulula kumwamba, ndi
zonse za m'menemo, ndinazilamulira ndine. 13Ine ndautsa Koresi
m'cilungamo, ndipo ndidzalungamitsa njira zace zonse; iye
adzamanga mudzi wanga, nadzaleka andende anga anke mwa
ufulu, wosati ndi mtengo pena mphotho, ati Yehova wa makamu.
14Atero Yehova, Nchito ya Aigupto, ndi malonda a Kusi, ndi a
Sabea, amuna amsinkhu adzakugonjera, nadzakhala ako;
nadzakutsata pambuyo m'maunyolo; adzakugonjera,
nadzakugwira; adzakupembedza ndi kunena, Zoona Mulungu ali
mwa iwe; ndipo palibenso wina, palibe Mulungu. 15Ndithu Inu
ndinu Mulungu, amene mudzibisa nokha, Mulungu wa Israyeli,

Mpulumutsi. 16Iwo adzakhala ndi manyazi, inde, adzathedwa nzeru
onsewo; adzalowa m'masokonezo pamodzi, amene apanga
mafano. 17Koma Israyeli adzapulumutsidwa ndi Yehova ndi
cipulumutso cosatha; inu simudzakhala ndi manyazi, pena
kuthedwa nzeru ku nthawi zosatha.
18Pakuti atero Yehova amene analenga kumwamba, Iye ndiye
Mulungu amene anaumba dziko lapansi, nalipanga; Iye
analikhazikitsa, sanalilenga mwacabe; Iye analiumba akhalemo
anthu; Ine ndine Yehova; ndipo palibenso wina. 19Ine sindinanena
m'tseri m'malo a dziko la mdima; Ine sindinati kwa mbeu ya
Yakobo, Mundifune Ine mwacabe; Ine Yehova ndinena cilungamo,
ndinena zimene ziri zoona. 20Sonkhanani nokha, mudze;
yandikirani cifupi pamodzi, inu amene mwapulumuka amitundu;
iwo alibe nzeru, amene anyamula mtengo wa fano lao losema, ndi
kupemphera mlungu wosakhoza kupulumutsa. 21Nenani inu,
turutsani mlandu wanu; inde, acite uphungu pamodzi; ndani
waonetsa ici ciyambire nthawi yakale? ndani wanena ici kale? kodi
si ndine Yehova? ndipo palibenso Mulungu wina popanda Ine;
Mulungu wolungama, ndi Mpulumutsi; palibenso wina popanda
Ine. 22Yang'anani kwa Ine, mupulumutsidwe, inu malekezero onse
a dziko; pakuti Ine ndine Mulungu, palibe wina. 23Ndadzilumbira
ndekha, mau acokera m'kamwa mwanga m'cilungamo, ndipo
sadzabwerera, kuti mabondo onse adzandigwadira Ine, malilime
onse nadzalumbira Ine. 24Koma mwa Yehova yekha, wina adzati
kwa Ine, muli cilungamo ndi mphamvu; ngakhale kwa Iyeyo anthu
adzafika, ndi onse amene anamkwiyira, adzakhala ndi
manyazi. 25Mwa Yehova mbeu yonse ya Israyeli idzalungamitsidwa
ndi 7 kudzikuza.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Aneneratu za kupasuka kwa mafano a ku Babulo

1Beli agwada pansi, Nebo awerama; mafano ao ali pa zoweta, ndi
pa ng'ombe; zinthu zimene inu munanyamula ponseponse
ziyesedwa mtolo, katundu wakulemetsa nyama. 2Milunguyo
iwerama, igwada pansi pamodzi; singapulumutse katundu, koma
iyo yeni yalowa m'ndende.
3Mverani Ine, banja la Yakobo, ndi otsala onse a banja la Israyeli,
amene ndakunyamulani kuyambira m'mimba, ndi kukusenzani
cibadwire; 4ngakhale mpaka mudzakalamba Ine ndine, ndipo
ngakhale mpaka tsitsi laimvi, Ine ndidzakusenzani inu; ndalenga,
ndipo ndidzanyamula; inde, ndidzasenza, ndipo
ndidzapulumutsa. 5Kodi mudzandifanizira ndi yani, ndi
kundilinganiza ndi kundiyerekeza, kuti ife tifanane? 6Amene ataya
golidi, namturutsa m'thumba, ndi kuyesa siliva ndi muyeso, iwo
alemba wosula golidi; iye napanga nazo mlungu; iwo agwada
pansi, inde alambira. 7Iwo amanyamula mlunguwu paphewa,
nausenza, naukhazika m'malo mwace, nukhala ciriri; pamalo
pacepo sudzasunthika; inde, wina adzaupfuulira, koma sungathe
kuyankha, kapena kumpulumutsa m'zobvuta zace.
8Kumbukirani ici, nimucirimike, mudzikumbutsenso, olakwa
inu. 9Kumbukirani zinthu zoyamba zakale, kuti Ine ndine Mulungu,
ndipo palibenso wina; Ine ndine Yehova, ndipo palibenso wina
wofana ndi Ine; 10ndilalikira za cimariziro kuyambira paciyambi, ndi
kuyambira nthawi zakale ndinena zinthu zimene zisanacitidwe; ndi
kunena, Uphungu wanga udzakhala, ndipo ndidzacita zofuna zanga
zonse; 11ndiitana mbalame yolusa kucokera kum'mawa, ndiye
munthu wa uphungu wanga, kucokera ku dziko lakutari; inde,
ndanena, ndidzacionetsa; ndinatsimikiza mtima,
ndidzacicitanso. 12Mverani Ine, inu olimba mtima, amene muli
kutari ndi cilungamo; 13ndiyandikizitsa cifupi cilungamo canga
sicidzakhala patari, ndipo cipulumutso canga sicidzacedwa; ndipo
ndidzaika cipulumutso m'Ziyoni, ca kwa Israyeli ulemerero wanga.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Babulo adzaonongeka konse

1Tsika, ukhale m'pfumbi, namwaliwe, mwana wamkazi wa Babulo;
khala pansi popanda mpando wacifumu, mwana wamkazi wa
Akasidi, pakuti iwe sudzayesedwanso wozizira ndi
wololopoka. 2Tenga mipero, nupere ufa; cotsa cophimba cako,
bvula copfunda, kwinda m'mwendo, oloka mitsinje. 3Marisece ako
adzakhala osapfundidwa, inde, manyazi ako adzaoneka; ndidzacita
kubwezera, osasamalira munthu. 4Mombolo wathu, Yehova wa
makamu ndi dzina lace, Woyera wa Israyeli. 5Khala iwe cete, lowa
mumdima, mwana wamkazi wa Akasidi; pakuti sudzachedwanso
mkazi wa maufumu. 6Ndinakwiyira anthu anga, ndinaipitsa colowa
canga, ndi kuwapereka m'manja ako; koma iwe sunawaonetsera
cifundo; wasenzetsa okalamba goli lako lolemera ndithu. 7Ndipo
unati, Ndidzakhala mkazi wa mfumu wa nthawi zonse; ndipo
sunasamalira izi mumtima mwako, kapena kukumbukira comarizira
cace.
8Cifukwa cace tsono, imva ici, iwe wotsata zokondweretsa, amene
umakhala mosatekeseka, amene umati mumtima mwako, Ine
ndine, ndipo popanda ine palibenso wina; sindidzakhala monga
mkazi wamasiye, kapena kudziwa kumwalira kwa ana; 9koma izi
ziwiri zidzakugwera mwadzidzidzi, tsiku limodzi kumwalira kwa ana
ndi umasiye zidzakugwera; mokwanira monse, pakati pa unyinji wa
matsenga ako, ndi pakati pa maphenda ako ambirimbiri. 10Pakuti
wakhulupirira zoipa zako, wati, Palibe wondiona ine; nzeru zako ndi
cidziwitso cako zakusandutsa woipa; ndipo wanena mumtima
mwako, Ndine, ndipo popanda ine palibenso wina. 11Cifukwa cace
coipa cidzafika pa iwe; sudzadziwa kuca kwace, ndipo cionongeko
cidzakugwera; sudzatha kucikankhira kumbali; ndipo cipasuko
cosacidziwa iwe cidzakugwera mwadzidzidzi. 12Taima tsopano ndi
maphendo ako, ndi unyinji wa matsenga ako, m'menemo iwe
unagwira nchito ciyambire ubwana wako; kuti kapena udzatha
kupindula, kuti kapena udzapambana. 13Watopa mu uphungu wako
wambiri; aimirire tsopano openda zam'mwamba, oyang'ana
nyenyezi, akuneneratu mwezi ndi mwezi, ndi kukupulumutsa pa
zinthu zimene zidzakugwera. 14Taona, iwo adzakhala ngati ziputu,
moto udzawatentha iwo; sadzadzipulumutsa okha ku mphamvu za
malawi; motowo sudzakhala khala loothako, pena moto
wakukhalako. 15Zinthu zomwe unagwira nchito yace, zidzatero
nawe; iwo amene anacita malonda ndi iwe ciyambire pa ubwana
wako, adzayenda yense kunka kumalo kwace; sipadzakhala
wopulumutsa iwe.

Awadandaulira Aisrayeli, awacenteza, nalonjezana nao

1Imvani inu ici, banja la Yakobo, amene muchedwa ndi dzina la
Israyeli, amene munaturuka m'madzi a Yuda amene mulumbira
dzina la Yehova ndi kuchula dzina la Mulungu wa Israyeli, koma si
m'zoona, pena m'cilungamo. 2Pakuti adziyesa okha a mudzi
wopatulika, ndi kudzikhazikitsa iwo okha pa Mulungu wa Israyeli;
dzina lace ndi Yehova wa makamu. 3Ndanena zinthu zoyamba
kuyambira kale; inde, izo zinaturuka m'kamwa mwanga, ndipo
ndinazisonyeza; mwadzidzidzi ndinazicita izo, ndipo
zinaoneka. 4Popeza ndinadziwa, kuti uli wokanika, ndi khosi lako liri
mtsempha wacitsulo, ndi mphumi yako mkuwa; 5cifukwa cace
ndinakudziwitsa ici kuyambira kale; cisanaoneke ndinakusonyeza
ico, kuti iwe unganene, Fano langa lacita izo, ndi cifanizito canga
cosema, ndi cifaniziro canga coyenga zinazilamulira. 6Iwe wacimva
taona zonsezi; ndipo inu kodi inu simudzacinena? Ndakusonyeza
iwe zinthu zatsopano kucokera nthawi yino, ngakhale zinthu
zobisika, zimene iwe sunazidziwe. 7Zalengedwa tsopano, zosati
kuyambira kale; ndipo lisanafike tsiku laleroli iwe sunazimve;
unganene, Taonani, ndinazidziwa. 8Inde, iwe sunamva; inde,
sunadziwe; inde, kuyambira kale khutu lako silinatsegudwe; pakuti
ndinadziwa kuti iwe wacita mwaciwembu ndithu, ndipo
unayesedwa wolakwa cibadwire. 9Cifukwa ca dzina langa
ndidzacedwetsa mkwiyo wanga, ndi cifukwa ca kutamanda kwanga
ndidzakulekerera, kuti ndisakucotse. 10Taona ndakuyenga, koma si
monga siliva, ndakuyesa iwe m'ng'anjo ya masautso. 11Cifukwa ca
Ine ndekha, cifukwa ca Ine ndekha ndidzacita ici, pakuti dzina
langa lidetsedwerenji? ndi ulemerero wanga sindidzaupereka kwa
wina.
12Mverani Ine, Yakobo ndi Israyeli, oitanidwa anga, Ine ndine; ndine
woyamba, Inenso ndine womariza. 13Inde dzanja langa linakhazika
maziko a dziko lapansi, ndi dzanja langa lamanja linafunyulula
m'mwamba; pakuziitana Ine ziimirira pamodzi. 14Sonkhanani inu
nonse ndi kumva, ndani mwa iwo aonetsa zinthu izi? Iye amene
Yehova anamkonda, iye adzacita kufuna kwace pa Babulo, ndi
mkono wace udzakhala pa Akasidi. 15Ine, ngakhale Ine ndanena;
inde ndamwitana iye, ndamfikitsa, ndipo adzapindula nayo njira
yace. 16Idzani inu cifupi ndi Ine, imvani ici; kuyambira pa ciyambi
sindinanene m'tseri; ciyambire zimenezi, Ine ndiripo; ndipo
tsopano Ambuye Mulungu wanditumiza Ine ndi mzimu
wace. 17Atero Yehova, Mombolo wako, Woyera wa Israyeli, Ine
ndine Yehova, Mulungu wako, amene ndikuphunzitsa kupindula,
amene ndikutsogolera m'njira yoyenera iwe kupitamo. 18Mwenzi

utamvera malamulo anga mtendere wako ukanakhala ngati
mtsinje, ndi cilungamo cako monga mafunde a nyanja; 19mbeu
yakonso ikadakhala monga mcenga ndi obadwa a m'cuuno mwako
momwemo; dzina lace silikadacotsedwa, pena kuonongeka
pamaso panga.
20Turukani inu m'Babulo, athaweni Akasidi; ndi mau akuyimba
nenani inu, bukitsani ici, lalikirani ici, ngakhale ku malekezero a
dziko; nenani, Yehova waombola mtumiki wace Yakobo. 21Ndipo
iwo sanamva ludzu, pamene Iye anawatsogolera m'mapululu;
anawaturutsira madzi kuturuka m'matanthwe; anadulanso
thanthwe, madzi nabulika. 221 Kulibe mtendere, ati Yehova, kwa
oipa.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Mtumiki wa Yehova, kuunika kwa amitundu

1Mverani Ine, zisumbu inu, mumvere anthu inu akutari; Yehova
anandiitana Ine ndisanabadwe; m'mimba mwa amai Iye anachula
dzina langa; 2nacititsa pakamwa panga ngati lupanga lakuthwa,
mu mthunzi wa dzanja lace wandibisa Ine; wandipanga Ine mubvi
wotuulidwa; m'phodo mwace Iye wandisungitsa Ine, nati kwa
Ine, 3Iwe ndiwe mtumiki wanga, Israyeli, amene
ndidzalemekezedwa nawe. 4Koma ndinati, Ndagwira nchito
mwacabe, ndatha mphamvu zanga pacabe, ndi mopanda pace;
koma ndithu ciweruziro canga ciri ndi Yehova, ndi kubwezera
kwanga kuli ndi Mulungu wanga. 5Ndipo tsopano, ati Yehova,
amene anandiumba Ine ndisanabadwe ndikhale mtumiki wace,
kubwezanso Yakobo kwa Iye, ndi kuti Israyeli asonkhanidwe kwa
Iye; cifukwa Ine ndiri wolemekezeka pamaso pa Yehova, ndipo
Mulungu wanga wakhala mphamvu zanga; 6inde, ati, Ciri cinthu
copepuka ndithu kuti Iwe ukhale mtumiki wanga wakuutsa mafuko
a Yakobo, ndi kubwezera osungika a Israyeli; ndidzakupatsanso
ukhale kuunika kwa amitundu, kuti ukhale cipulumutso canga
mpaka ku malekezero a dziko lapansi. 7Atero Yehova, Mombolo wa
Israyeli, ndi Woyera wace, kwa Iye amene anthu amnyoza, kwa Iye
amene mtundu wathu unyansidwa naye, kwa mtumiki wa
olamulira: Mafumu adzaona, nadzauka; akalonga nadzalambira
cifukwa ca Yehova, amene ali wokhulupirika, ngakhale Woyera wa
Israyeli, amene anakusankha Iwe. 8Atero Yehova, Nthawi
yondikomera ndakuyankha Iwe, ndi tsiku la cipulumutso
ndakuthandiza; ndipo ndidzakusunga ndi kupatsa Iwe ukhale
pangano la anthu, kuti ukhazikitse dziko, nuwalowetse m'zolowa
zopasuka m'malo abwinja; 9ndi kunena kwa iwo amene ali
omangidwa, Mukani, kwa iwo amene ali mumdima, Dzionetseni
nokha. Iwo adzadya m'njira, ndi m'zitunda zonse zoti se
mudzakhala busa lao. 10Iwo sadzakhala ndi njala, pena ludzu;
ngakhale thukuta, pena dzuwa silidzawatentha; pakuti Iye amene
wawacitira cifundo, adzawatsogolera, ngakhale pa akasupe a
madzi adzawatsogolera. 11Ndipo ndidzasandutsa mapiri anga onse
akhale njira, ndipo makwalala anga adzakwezeka. 12Taonani, awa
adzacokera kutari; ndipo taonani, awa ocokera kumpoto, ndi
kumadzulo; ndi awa ocokera ku dziko la Sinimu. 13Yimbani inu,
m'mwamba, nukondwere iwe dziko lapansi, yimbani inu mapiri,
pakuti Yehova watonthoza mtima wa anthu ace, nadzacitira
cifundo obvutidwa ace.
14Koma Ziyoni anati, Yehova wandisiya ine, ndipo Ambuye
wandiiwala ine. 15Kodi mkazi angaiwale mwana wace wa pabere,

kuti iye sangacitire cifundo mwana wombala iye? inde awa angaiwale, koma Ine sindingaiwale iwe. 16Taona ndakulembera iwe pa zikhato za manja anga; makoma ako alipo masiku onse pamaso panga, 17Ana ako afulumira; opasula ako ndi iwo amene anakusakaza adzacoka pa iwe. 18Tukula maso ako kuunguza-unguza, nuone; onsewa asonkhana pamodzi, nadza kwa iwe. Pali Ine, ati Yehova, iwe ndithu udzadzibveka wekha ndi iwo onse, monga ndi cokometsera, ndi kudzimangira nao m'cuuno ngati mkwatibwi. 19Pakuti, kunena za tnalo ako osiyidwa ndi abwinja ndi dziko lako limene lapasulidwa tsopano, ndithu iwe udzakhala wocepera okhalamo, ndi iwo amene anakumeza iwe adzakhala kutari. 20Ana ako amasiye adzanena m'makutu ako, Malo andicepera ine, ndipatse malo, kuti ndikhalemo. 21Pamenepo udzati m'mtima mwako, Ndani wandibalitsa ine amenewa, popeza ana anga anacotsedwa kwa ine, ndipo ndiri wouma, ndi wocotsedwa m'dziko, ndi woyendayenda kwina ndi kwina? ndipo ndani wadza ndi awa? Taona ndinasiyidwa ndekha, amenewa anali kuti?
22Atero Ambuye Yehova, Taona ndidzakodola anthu a mitundu, ndi kukwezera anthu mbendera yanga; ndipo adzabwera nao ana ako amuna pa cifuwa cao, ndi ana ako akazi adzatengedwa pa mapewa ao. 23Ndipo mafumu adzakulera, ndi akazi ao akuru adzakuyamwitsa; iwo adzakugwadira ndi nkhope zao zoyang'ana pansi, nadzaseteka pfumbi la m'mapazi ako: ndipo iwe udzadziwa kuti Ine ndine Yehova, ndi iwo amene alindira Ine sadzakhala ndi manyazi. 24Kodi cofunkha cingalandidwe kwa wamphamvu, pena am'nsinga a woopsya angapulumutsidwe? 25Koma atero Yehova, Ngakhale am'nsinga a wamphamvu adzalandidwa, ndi cofunkha ca woopsya cidzapulumutsidwa; pakuti Ine ndidzakangana naye amene akangana ndi iwe, ndipo ndidzapulumutsa ana ako. 26Ndipo ndidzadyetsa iwo amene atsendereza iwe ndi nyama yao yao; ndi mwazi wao wao; iwo adzaledzera monga ndi vinyo wotsekemera; anthu onse adzadziwa kuti Ine Yehova ndiri Mpulumutsi wako, ndi Mombolo wako, Wamphamvu wa Yakobo.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Mtumiki wa Yehova anyozedwa koma athandizidwa

1Atero Yehova, Kalata wa cilekaniro ca amako ali kuti amene
ndinamsudzula naye? pena ndani wa angongole anga amene
ndamgulitsa iwe? Taona cifukwa ca zoipa zanu munagulitsidwa, ndi
cifukwa ca kulakwa kwanu amanu anacotsedwa. 2Cifukwa canji
ndinafika osapeza munthu? ndi kuitana koma panalibe wina
woyankha? Kodi dzanja langa lafupika konse, kuti silingathe
kuombola? pena Ine kodi ndilibe mphamvu zakupulumutsa? Taona
pa kudzudzula kwanga ndiumitsa nyanja yaikuru, ndi kusandutsa
mitsinje cipululu; nsomba zace zinunkha cifukwa mulibe madzi,
nizifa ndi ludzu. 3Ndibveka thambo ndi kuda, ndi kuyesa ciguduli
copfunda cace.
4Ambuye Yehova wandipatsa Ine lilime la ophunzira, kuti ndidziwe
kunena mau akucirikiza iye amene ali wolema. Iye andigalamutsa
m'mawa ndi im'mawa, nagalamutsa khutu langa kuti limve monga
ophunzira. 5Ambuye Yehova watsegula khutu langa, ndipo
sindinakhala wopanduka ngakhale kubwerera
m'mbuyo. 6Ndinapereka msana wanga kwa omenya, ndi masaya
anga kwa iwo amene anakudzula tsitsi langa; sindinabisira nkhope
yanga manyazi ndi kulabvulidwa. 7Pakuti Ambuye Yehova
adzandithangata Ine; cifukwa cace sindinasokonezedwa; cifukwa
cace ndakhazika nkhope yanga ngati mwala, ndipo ndidziwa kuti
sindidzakhala ndi manyazi. 8Iye ali pafupi amene alungamitsa Ine;
ndani adzakangana ndi Ine? tiyeni tiimirire tonse pamodzi; mdani
wanga ndani? andiyandikire. 9Taonani, Ambuye Yehova
adzathandiza Ine; ndani amene adzanditsutsa? taonani, iwo onse
adzatha ngati cobvala, njenjete zidzawadya.
10Ndani ali mwa inu amene amaopa Yehova, amene amamvera
mau a mtumiki wace? Iye amene ayenda mumdima, ndipo alibe
kuunika, akhulupirire dzina la Yehova, ndi kutsamira Mulungu
wace. 11Taonani, inu nonse amene muyatsa moto, amene
mudzimangira m'cuuno ndi nsakali, yendani inu m'cirangati ca
moto wanu, ndi pakati pa nsakali zimene mwaziyatsa. Ici
mudzakhala naco ca pa dzanja langa; mudzagona pansi ndi cisoni.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Israyeli akonzedwanso napulumutsidwa

1Mverani Ine, inu amene mutsata cilungamo, inu amene mufuna
Yehova; yang'anani ikuthanthwe, kumene inu munasemedwamo,
ndi kuuna kwa dzenje, kumene inu munakumbidwamo. 2Yang'anani
kwa Abrahamu kholo lanu, ndi kwa Sara amene anakubalani inu;
pakuti pamene iye anali mmodzi yekha ndinamuitana iye; ndipo
ndinamdalitsa ndi kumcurukitsa. 3Pakuti Yehova watonthoza mtima
wa Ziyoni, watonthoza mtima wa malo ace onse abwinja; ndipo
wasandutsa cipululu cace ngati Edene, ndi nkhwangwara yace
ngati munda wa Yehova; kukondwa ndi kusangalala kudzapezedwa
m'menemo, mayamikiro, ndi mau a nyimbo yokoma.
4Mverani Ine, inu anthu anga, ndi kundicherera makutu, iwe,
mtundu wa anthu anga; pakuti lamulo lidzacokera kwa ine, ndipo
ndidzakhazikitsa ciweruziro canga cikhale kuunika kwa
anthu. 5Cilungamo canga ciripafupi, cipulumutso canga camuka;
ndipo mikono yanga idzaweruza anthu; zisumbu zidzandilindira,
ndipo adzakhulupirira mkono wanga. 6Tukulani maso anu
kumwamba, ndipo muyang'ane pansi pa dziko; pakuti kumwamba
kudzacoka ngati utsi, ndi dziko lidzatha ngati copfunda, ndipo iwo
amene akhala m'menemo adzafa cimodzimodzi; koma cipulumutso
canga cidzakhala ku nthawi lonse, ndi cilungamo canga
sicidzacotsedwa.
7Mverani Ine, inu amene mudziwa cilungamo, anthu amene
mumtima mwao muli lamulo langa; musaope citonzo ca anthu,
ngakhale kuopsedwa ndi kutukwana kwao. 8Pakuti njenjete
idzawadya ngati copfunda, ndi mbozi zidzawadya ngati ubweya;
koma cilungamo canga cidzakhala ku nthawi zonse, ndi
cipulumutso canga ku mibadwo yonse.
9Galamuka, galamuka, khala ndi mphamvu, mkono wa Yehova;
galamuka monga masiku akale, mibadwo ya nthawi zakale. Kodi si
ndiwe amene unadula Rahabu zipinjiri zipinjiri, amene unapyoza
cinjoka cija? 10Kodi si ndiwe amene unaumitsa nyanja, madzi
akuya kwambiri; amene anasandutsa nyanja zikhale njira ya
kupitapo oomboledwa? 11Ndipo oomboledwa a Yehova adzabwera,
nadzafika ku Ziyoni; ndi nyimbo ndi kukondwa kosatha kudzakhala
pa mitu yao; adzakhala m'kusangalala ndi kukondwa, ndipo cisoni
ndi kuusa moyo kudzacoka.
12Ine, Inedi, ndine amene nditonthoza mtima wako; kodi iwe ndani,
kuti uopa munthu amene adzafa, ndi mwana wa munthu amene
adzakhala ngati udzu; 13waiwala Yehova Mlengi wako, amene
anayala m'mwamba, nakhazika maziko a dziko lapansi, ndi
kuopabe tsiku lonse cifukwa ca ukali wa wotsendereza, pamene iye

akonzeratu kupasula? uli kuti ukali wa
wotsendereza? 14Wam'nsinga wowerama adzamasulidwa
posacedwa; sadzafa ndi kutsikira kudzenje, cakudya cace
sicidzasowa. 15Pakuti Ine ndine Yehova Mulungu wako, amene
ndiutsa nyanja, kuti mafunde ace akokome; Yehova wa makamu
ndi dzina lace. 16Ndipo ndaika mau anga m'kamwa mwako; ndipo
ndakuphimba ndi mthunzi wa dzanja langa, kuti ndikhazike
kumwamba ndi kuika maziko a dziko lapansi, ndi kunena kwa
Ziyoni, Inu ndinu anthu anga.

Agalamuke Yerusalemu

17Galamuka, galamuka, imirira Yerusalemu amene unamwa
m'dzanja la Yehova cikho ca ukali wace; iwe wamwa mbale ya
cikho conjenjemeretsa ndi kucigugudiza. 18Palibenso wina
wakumtsogolera mwa ana amuna onse, amene iye anawabala;
palibe wina amgwira dzanja mwa ana onse anawalera. 19Izi ziwiri
zakugwera; ndani adzakulira iwe? bwinja ndi cipasuko, njala ndi
lupanga; ndidzatonthoza mtima wako bwanji? 20Ana ako amuna
akomoka; agona pamtu pa makwalala onse, monga nswala
muukonde; adzala ndi ukali wa Yehova, kudzudzula kwa Mulungu
wako, 21Cifukwa cace imva ici tsopano, iwe wobvutidwa ndi
woledzera koma si ndi vinyo ai; 22atero Ambuye ako Yehova, ndi
Mulungu wako amene anena mlandu wa anthu ace, Taona,
ndacotsa m'dzanja mwako cikho conjenjemeretsa, ngakhale mbale
ya cikho ca ukali wanga; iwe sudzamwa ico
kawirinso. 23Ndidzaciika m'dzanja la iwo amene abvutitsa iwe;
amene anena ku moyo wako, Gwada pansi kuti ife tipite; ndipo iwe
wagonetsa pamsana pako monga pansi, ndi monga khwalala kwa
iwo amene apita pamenepo.

©The Bible Society of Malawi, 1992

1Galamuka galamuka, tabvala mphamvu zako, Ziyoni; tabvala
zobvala zako zokongola, Yerusalemu, mzinda wopatulika; pakuti
kuyambira tsopano sadzalowanso kwa iwe wosadulidwa ndi
wodetsedwa. 2Dzisanse pfumbi; uka, khala tsonga, Yerusalemu;
udzimasulire maunyolo a pakhosi pako, iwe mwana wamkazi
wam'nsinga wa Ziyoni.

3Pakuti atero Yehova, Inu munagulitsidwa cabe, ndipo
mudzaomboledwa opanda ndalama. 4Pakuti Ambuye Yehova atero,
Anthu anga ananka ku Aigupto poyamba paja, kukakhala
kumeneko; ndipo Asuri anawatsendereza popanda
cifukwa. 5Cifukwa cace kodi ndicitenji pano? ati Yehova; popeza
anthu anga acotsedwa popanda kanthu? akuwalamulira awaliritsa,
ati Yehova; ndipo dzina langa licitidwa mwano tsiku lonse
kosalekeza. 6Cifukwa cace anthu anga adzadziwa dzina langa;
cifukwa cacersiku limenelo iwo adzadziwa kuti Ine ndine amene
ndinena; taonani, ndine pano.
7Ha, akongolatu pamapiri mapazi a iye amene adza ndi uthenga
wabwino, amene abukitsa mtendere, amene adza ndi uthenga
wabwino wa zinthu zabwino, amene abukitsa cipulumutso; amene
ati kwa Ziyoni, Mulungu wako ndi mfumu. 8Mau a alonda ako!
akweza mau, ayimba pamodzi; pakuti adzaona maso ndi maso,
pamene Yehova abwerera kudza ku Ziyoni. 9Kondwani zolimba,
yimbani pamodzi, inu malo abwinja a pa Yerusalemu; pakuti
Yehova watonthoza mtima wa anthu ace, waombola
Yerusalemu. 10Yehova wabvula mkono wace woyera pamaso pa
amitundu onse; ndi malekezero onse a dziko lapansi adzaona
cipulumutso ca Mulungu wathu. 11Cokani inu, cokani inu, turukani
ku Babulo; musakhudze kanthu kodetsa; turukani pakati pace,
khalani okonzeka, inu amene munyamula zotengera za
Yehova. 12Pakuti simudzacoka mofulumira, kapena kunka
mothawa; pakuti Yehova adzakutsogolerani, ndi Mulungu wa
Israyeli adzadikira pambuyo panu.
13Taonani, Mtumiki wanga adzacita mwanzeru; adzakwezedwa ndi
kutukulidwa pamwamba, nadzakhala
pamwambamwamba. 14Monga ambiri anazizwa ndi iwe Israyeli,
momwemo nkhope yace yaipitsidwa ndithu, kupambana munthu
ali yense, ndi maonekedwe ace kupambana ana a
anthu; 15momwemonso Iye adzawazawaza mitundu yambiri;
mafumu adzamtsekera Iye pakamwa pao; pakuti cimene

sicinauzidwa kwa iwo adzaciona, ndi cimene iwo sanamva adzazindikira.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masomphenya a cisauko ndi ulemerero wa Mtumiki wa Yehova

1Ndani wamvera uthenga wathu? Ndi mkono wa Yehova
wabvumbulukira yani? 2Pakuti ameneyo adzaphuka pamaso pace
ngati mtengo wanthete, ndi ngati muzu womera m'nthaka youma;
Iye alibe maonekedwe, pena kukongola; ndipo pamene timuona
palibe kukongola kuti timkhumbe. 3Iye ananyozedwa ndi
kukanidwa ndi anthu; munthu wazisoni, ndi wodziwa zowawa;
ndipo ananyozedwa monga munthu wombisira anthu nkhope zao;
ndipo ife sitinamlemekeza.
4Zoonadi Iye ananyamula zowawa zathu, ndi kusenza zisoni zathu;
koma ife tinamuvesa wokhomedwa wokanthidwa ndi Mulungu, ndi
wobvutidwa. 5Koma Iye analasidwa cifukwa ca zolakwa zathu,
natundudzidwa cifukwa ca mphulupulu zathu; cilango cotitengera
ife mtendere cinamgwera Iye; ndipo ndi mikwingwirima yace ife
taciritsidwa. 6Tonse tasocera ngati nkhosa; tonse tayenda yense
m'njira ya mwini yekha; ndipo Yehova anaika pa Iye mphulupulu ya
ife tonse.
7Iye anatsenderezedwa koma anadzicepetsa yekha osatsegula
pakamwa pace; ngati nkhosa yotsogoleredwa kukaphedwa, ndi
ngati mwana wa nkhosa amene ali du pamaso pa omsenga,
motero sanatsegula pakamwa pace. 8Anacotsedwa ku cipsinjo ndi
ciweruziro; ndipo ndani adzafotokoza nthawi ya moyo wace? pakuti
walikhidwa kunja kuno; cifukwa ca kulakwa kwa anthu anga Iye
anakhomedwa. 9Ndipo anaika manda ace pamodzi ndi oipa, ndi
pamodzi ndi olemera mu imfa yace, ngakhale Iye sanacita ciwawa,
ndipo m'kamwa mwace munalibe cinyengo.
10Koma kunakomera Yehova kumtundudza; anammvetsa zowawa;
moyo wace ukapereka nsembe yoparamula, Iye adzaona mbeu
yace, adzatanimphitsa masiku ace; ndipo comkondweretsa Yehova
cidzakula m'manja mwace. 11Iye adzaona zotsatira mabvuto a
moyo wace, nadzakhuta nazo; ndi nzeru zace mtumiki wanga
wolungama adzalungamitsa ambiri, nadzanyamula mphulupulu
zao. 12Cifukwa cace ndidzamgawira gawo ndi akuru; ndipo
adzagawana ndi amphamvu zofunkha; pakuti Iye anathira moyo
wace kuimfa; ndipo anawerengedwa pamodzi ndi olakwa; koma
ananyamula macimo a ambiri, napembedzera olakwa.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Zokoma zimene Yehova adzacitira Mpingo wao

1Yimba, iwe wouma, amene sunabala; yimba zolimba ndi kupfuula
zolimba, iwe amene sunabala mwana; pakuti ana a mfedwa
acuruka koposa ana a mkazi wokwatibwa ndi mwamuna, ati
Yehova. 2Kuza malo a hema wako, afunyulule zinsaru za
mokhalamo iwe; usaleke, tanimphitsa zingwe zako, limbitsa
zikhomo zako. 3Pakuti iwe udzafalikira ponse pa dzanja lamanja ndi
lamanzere, ndipo mbeu yako idzalandira amitundu colowa cao, ndi
kukhalitsa anthu m'mabwinja. 4Usaope, pakuti sudzakhala ndi
manyazi; usasokonezedwe, pakuti sudzacitidwa manyazi; pakuti
udzaiwala manyazi a ubwana wako, ndi citonzo ca umasiye wako
sudzacikumbukiranso. 5Pakuti Mlengi wako ndiye mwamuna wako;
Yehova wa makamu ndiye dzina lace; ndi Woyera wa Israyeli ndiye
Mombolo wako; Iye adzachedwa Mulungu wa dziko lonse
lapansi. 6Pakuti Yehova wakuitana iwe monga mkazi wakusiyidwa
ndi wosauka m'mzimu, ngakhale mkazi wa ubwana wocotsedwa,
ati Mulungu wako. 7Kamphindi kakang'ono ndakusiya iwe, koma
ndi cifundo cambiri ndidzakusonkhanitsa. 8M'kukwiya kwa
kusefukira ndinakubisira nkhope yanga kamphindi; koma ndi
kukoma mtima kwa cikhalire ndidzakucitira cifundo, ati Yehova
Mombolo wako. 9Pakuti kumeneku kuli kwa Ine monga madzi a
Nowa; pakuti monga ndinalumbira kuti madzi a Nowa
sadzamizanso pa dziko lapansi, momwemo ndinalumbira kuti
sindidzakukwiyira iwe, pena kukudzudzula. 10Pakuti mapiri
adzacoka, ndi zitunda zidzasunthika; koma kukoma mtima kwanga
sikudzakucokera iwe, kapena kusunthika cipangano canga ca
mtendere, ati Yehova amene wakucitira iwe cifundo.
11Iwe wosautsidwa, wobelukabeluka ndi namondwe, wosatonthola
mtima, taona, ndidzakhazika miyala yako m'maanga-maanga
abwino, ndi kukhazika maziko ako ndi masafiro. 12Ndipo
ndidzamanga mazenera ako ndi miyala yofiira, ndi zipata zako ndi
bareketi, ndi malire ako onse ndi miyala yokondweretsa. 13Ndipo
ana ako onse adzaphunzitsidwa ndi Yehova; ndipo mtendere wa
ana ako udzakhala waukulu. 14M'cilungamo iwe udzakhazikitsidwa,
udzakhala kutari ndi cipsinjo, pakuti sudzaopa; udzakhala kutari
ndi mantha, pakuti sadzafika cifupi ndi iwe. 15Taona, iwo
angasonkhanitse pamodzi, koma si ndi Ine; amene ali yense
adzasonkhana pamodzi akangane ndi iwe adzagwa cifukwa ca
iwe. 16Taona, ndalenga wacipala amene abvukuta moto wamakala,
ndi kuturutsamo cida ca nchito yace; ndipo ndalenga woononga
kuti apasule. 17Palibe cida cosulidwira iwe cidzapindula; ndipo
lilime lonse limene lidzakangana nawe m'ciweruzo udzalitsutsa. Ici

ndi colowa ca atumiki a Yehova, ndi cilungamo cao cimene cifuma kwa Ine, ati Yehova.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Osauka onse aitanidwa alandire cipulumutso

1Inu nonse, inu akumva ludzu, idzani kumadzi; ndi osowa ndarama
idzani inu mugule mudye; inde idzani, mugule vinyo ndi mkaka
opanda ndarama ndi opanda mtengo wace. 2Bwanji inu
mulikutayira ndarama cinthu cosadya, ndi kutayira malipiro anu
zosakhutitsa? Mverani Ine mosamalitsa, nimudye cimene ciri
cabwino, moyo wanu nubondwere ndi zonona. 3Cherani Lhutu
lanu, mudze kwa Ine, imvani, mzimu wanu nudzakhala ndi moyo;
ndipo ndidzapangana nanu cipangano cosatha, ndico zifundo
zoona za Davide. 4Taonani, ndampereka iye akhale mboni ya
anthu, wotsogolera ndi wolamulira anthu. 5Taona, iwe udzaitana
mtundu umene sunaudziwa, ndi mtundu umene sunakudziwa
udzakuthamangira, cifukwa ca Yehova Mulungu wako, ndi cifukwa
ca Woyera wa Israyeli; pakuti Iye wakukometsa.
6Funani Yehova popezeka Iye, itanani Iye pamene ali
pafupi; 7woipa asiye njira yace, ndi munthu wosalungama asiye
maganizo ace, nabwere kwa Yehova; ndipo Yehova adzamcitira
cifundo; ndi kwa Mulungu wathu, pakuti Iye adzakhululukira
koposa. 8Pakuti maganizo anga sali maganizo anu, ngakhale njira
zanu siziri njira zanga, ati Yehova. 9Pakuti monga kumwamba kuli
kutari ndi dziko lapansi, momwemo njira zanga ziri zazitari
kupambana njira zanu, ndi maganizo anga kupambana maganizo
anu. 10Pakuti monga mvula imagwa pansi ndi matalala, kucokera
kumwamba yosabwerera komweko, koma ikhamiza nthaka ndi
kuibalitsa, ndi kuiphukitsa, ndi kuipatsitsa mbeu kwa wobzyala, ndi
cakudya kwa wakudya; 11momwemo adzakhala mau anga amene
aturuka m'kamwa mwanga, sadzabwerera kwa Ine cabe, koma
adzacita cimene ndifuna, ndipo adzakula m'mene
ndinawatumizira. 12Pakuti inu mudzaturuka ndi kukondwa, ndi
kutsogozedwa ndi mtendere; mapiri ndi zitunda, zidzayimba
zolimba pamaso panu, ndi mitengo yonse ya m'thengo idzaomba
m'manja mwao. 13M'malo mwa mithethe mudzaturuka mtengo
wamlombwa; ndi m'malo mwa lunguzi mudzamera mtengo
wamcisu; ndipo cidzakhala kwa Yehova ngati mbiri, ngati
cizindikiro cosatha, cimene sicidzalikhidwa.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Malonjezo a kwa iwo osunga Sabata

1Atero Yehova, Sungani inu ciweruziro, ndi kucita cilungamo; pakuti
cipulumutso canga ciri pafupi kudza, ndi cilungamo canga ciri
pafupi kuti cib zumbulutsidwe, 2Wodala munthu amene acita ici,
ndi mwana wa munthu amene agwira zolimba ici, amene asunga
sabata osaliipitsa, nasunga dzanja lace osacita nalo coipa ciri
conse. 3Mlendo amene wadziphatika yekha kwa Yehova asanene,
kuti, Yehova adzandilekanitsa ndithu ndi anthu ace; pena mfule
asanene, Taonani ine ndiri mtengo wouma. 4Pakuti atero Yehova
kwa mifule imene isunga masabata, nisankha zinthu zimene
zindikondweretsa Ine, nigwira zolimba cipangano canga, 5Kwa iyo
ndidzapatsa m'nyumba yanga ndi m'kati mwa makoma anga malo,
ndi dzina loposa la ana amuna ndi akazi; ndidzawapatsa dzina
lacikhalire limene silidzadulidwa. 6Alendonso amene adziphatika
okha kwa Yehova, kuti amtumikire Iye, ndi kukonda dzina la
Yehova, akhale atumiki ace, yense amene asunga sabata
osaliipitsa, nagwira zolimba cipangano canga; 7naonso ndidzanka
nao ku phiri langa lopatulika, ndi kuwasangalatsa m'nyumba yanga
yopemphereramo; zopereka zao zopsereza ndi nsembe zao
zidzalandiridwa pa guwa la nsembe langa; pakuti nyumba yanga
idzachedwa nyumba yopemphereramo anthu onse. 8Ambuye
Yehova amene asonkhanitsa otayika a Israyeli ati, Komabe
ndidzasonkhanitsa ena kwa iye, pamodzi ndi osonkhanitsidwa ace
ace.
9Inu zirombo zonse za m'thengo, idzani kulusa, inde zirombo inu
nonse za m'nkhalango. 10Alonda ace ali akhungu, iwo onse ali
opanda nzeru; iwo onse ali agaru acete, osatha kuuwa; kungolota,
kugona pansi, kukonda kugona tulo. 11Inde agaru ali osusuka,
sakhuta konse; amenewa ali abusa osazindikira; iwo onse
atembenukira ku njira zao, yense kutsata phindu lace m'dera
lace. 12Idzani inu, ati iwo, ndidzatengera vinyo, ndipo tidzakhuta
cakumwa caukali; ndipo mawa kudzakhala monga tsiku lalero,
tsiku lalikuru loposa ndithu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Kupembedza mafano kwa Israyeli

1Wolungama atayika, ndipo palibe munthu wosamalirapo; ndipo
anthu acifundo atengedwa, palibe wolingalira kuti wolungama
acotsedwa pa coipa cirinkudza. 2Iye alowa mumtendere, iwo
apuma pa mphasa zao, yense woyenda moongoka.
3Koma sendererani kuno cifupi, inu ana amuna a watsenga, mbeu
yacigololo ndi yadama. 4Ndiye yani mudzikondweretsa momseka?
Ndani mulikumyasamira kukamwa, ndi kumturutsira lilime? Kodi
inu simuli ana akulakwa, mbeu yonama? 5Inu amene muutsa
zilakolako zanu pakati pa mathundu, patsinde pa mitengo yonse ya
gudugudu, amene mupha ana m'zigwa pansi pa mapanga a
matanthwe? 6Pakuti pa miyala yosalala ya m'cigwa pali gawo lako;
iyo ndiyo gawo lako; ndiyo imene unaitsanulirira nsembe yothira,
ndi kupereka nsembe yaufa. Kodi ndidzapembedzedwa pa zinthu
zimenezi? 7Pamwamba pa phiri lalitaritari unayala mphasa yako;
kumenekonso wakwera kukapereka nsembe. 8Ndi kumbuyo kwa
zitseko ndi mphuthu waimiritsa cikumbutso cako, pakuti
wadzionetsa wekha kwa wina, wosati kwa Ine; ndipo wakwerako,
wakuza mphasa yako, ndi kupangana nao pangano; unakonda
mphasa yao kumene unaiona. 9Ndipo unanka kwa mfumu,
utadzola mafuta ndi kucurukitsa zonunkhira zako; ndipo unatumiza
atumwi ako kutari; ndipo wadzicepetsa wekha kufikira kunsi ku
manda. 10Unatopa ndi njira yako yaitari; koma sunanene, Palibe
ciyembekezo; iwe wapeza moyo wa dzanja lako; cifukwa cace
sunalefuka. 11Ndipo ndi yani amene wamuopa ndi kucita naye
mantha, kuti wanama, osandikumbukira Ine, kapena
kundisamalira? Kodi Ine sindinakhala cete nthawi yambiri, ndipo
iwe sunandiopa Ine konse? 12Ndidzaonetsa cilungamo cako ndi
nchito zako sudzapindula nazo. 13Pamene pakupfuula iwe
akupulumutse amene unawasonkhanitsa; koma mphepo
idzawatenga, mpweya udzacotsa onse; koma iye amene
andikhulupirira Ine adzakhala ndi dziko, nadzakhala naco colowa
m'phiri langa lopatulika. 14Ndipo adzanena, Undani, undani,
konzani njira, cotsani cokhumudwitsa m'njira mwa anthu anga.
15Pakuti atero Iye amene ali wamtari wotukulidwa, amene akhala
mwacikhalire, amene dzina lace ndiye Woyera, Ndikhala m'malo
atari ndi oyera, pamodzi ndi yense amene ali wa mzimu wosweka
ndi wodzicepetsa, kutsitsimutsa mzimu wa odzicepetsa, ndi
kutsitsimutsa mtima wa osweka. 16Pakuti sindidzatsutsana ku
nthawi zonse, sindidzakwiya masiku onse; pakuti mzimu
udzalefuka pamaso pa Ine, ndi miyoyo imene
ndinailenga. 17Cifukwa ca kuipa kwa kusirira kwace ndinakwiya ndi

kummenya iye; ndinabisa nkhope yanga, ndipo ndinakwiya; ndipo iye anankabe mokhota m'njira ya mtima wace. 18Ndaona njira zace, ndipo ndidzamciritsa; ndidzamtsogoleranso, ndi kumbwezera iye ndi olira maliro ace zotonthoza mtima. 19Ndilenga cipatso ca milomo, Mtendere, mtendere kwa iye amene ali kutari, ndi kwa iye amene ali cifupi, ati Yehova; ndipo ndidzamciritsa iye. 20Koma oipa ali ofanana ndi nyanja yowinduka; pakuti siingapume, ndi madzi ace autsa matope ndi ubve. 21Palibe mtendere, ati Mulungu wanga, kwa oipa.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Kusala kosayenera, ndi kusala koyenera

1Pfuula zolimba, usalekerere, kweza mau ako ngati lipenga, ndi
kuwafotokozera anthu anga colakwa cao, ndi banja la Yakobo
macimo ao. 2Koma iwo andifuna Ine tsiku ndi tsiku, ndi kukondwera
kudziwa njira zanga; monga mtundu wa anthu ocita cilungamo,
osasiya cilangizo ca Mulungu wao, iwo andipempha Ine zilangizo
zolungama, nakondwerera kuyandikira kwa Mulungu. 3Amati,
Bwanji ife tasala kudya, ndipo Inu simuona? ndi bwanji ife
tabvutitsa moyo wathu, ndipo Inu simusamalira? Taonani, tsiku la
kusala kudya kwanu inu mupeza kukondwerera kwanu, ndi
kutsendereza anchito anu onse. 4Taonani, inu musala kudya kuti
mukangane ndi kutsutsana ndi kukantha ndi nkhonya yoipa; inu
simusala kudya tsiku lalero kuti mumveketse mau anu
kumwamba. 5Kodi kusala kudya koteroko ndiko ndinakusankha?
tsiku lakubvutitsa munthu moyo wace? Kodi ndiko kuweramitsa
mutu wace monga bango, ndi kuyala ciguduli ndi phulusa pansi
pace? Kodi uyesa kumeneko kusala kudya, ndi tsiku lobvomerezeka
kwa Yehova? 6Kodi kumeneku si kusala kudya kumene
ndinakusankha: kumasula nsinga za zoipa, ndi kumasula zomanga
gori, ndi kuleka otsenderezedwa amuke mfulu, ndi kuti mutyole
magori onse? 7Kodi si ndiko kupatsa cakudya cako kwa anjala, ndi
kuti ubwere nao kunyumba kwako aumphawi otayika? pakuona
wamalisece kuti umbveke, ndi kuti usadzibisire wekha a cibale
cako? 8Pomwepo kuunika kwako kudzawalitsa monga m'mawa, ndi
kucira kwako kudzaonekera msanga msanga; ndipo cilungamo
cako cidzakutsogolera; ulemerero wa Yehova udzakhala wocinjiriza
pambuyo pako. 9Pamenepo udzaitana, ndipo Yehova adzayankha;
udzapfuula ndipo Iye adzati, Ndine pano. Ngati ucotsa pakati pa
iwe gori, kukodolana moipa, ndi kulankhula moipa, 10ndipo ngati
upereka kwa wanjala cimene moyo Iwako umakhumba, ndi
kukhutitsa moyo wobvutidwa, pomwepo kuunika kwako kudzauka
mumdima, ndipo usiku wako udzanga usana; 11ndipo Yehova
adzakutsogolera posalekai, ndi kukhutitsa moyo wako m'cirala, ndi
kulimbitsa mafupa ako; ndipo udzafanana ndi munda wothirira
madzi, ndi kasupe wamadzi amene madzi ace saphwa
konse. 12Ndipo iwo amene adzakhala a iwe adzamanga malo akale
abwinja; udzautsa maziko a mibadwo yambiri; udzachedwa
Wokonza pogumuka, Wakubwezera njira zakukhalamo. 13Ukaletsa
phazi lako pa Sabata, ndi kusiya kucita kukondwerera kwako tsiku:
langa lopatulika, ndi kuyesa Sabata tsiku lokondwa lopatulika la
Yehova, lolemekezeka, ndipo ukalilemekeza ilo, osacita njira zako
zokha, osafuna kukondwa kwako kokha, osalankhula mau ako

okha; 14pomwepo udzakondwa mwa Yehova; ndipo Ine
ndidzakuyendetsa pa misanje ya dziko lapansi; ndipo
ndidzakudyetsa colowa ca kholo lako Yakobo; pakuti pakamwa pa
Yehova pananenapo.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Aulula zoipa za mtundu wao

1Taonani, mkono wa Yehova sufupika, kuti sungathe kupulumutsa;
khutu lace siliri logontha, kuti silingamve; 2koma zoipa zanu
zakulekanitsani inu ndi Mulungu wanu; ndipo macimo anu abisa
nkhope yace kwa inu, kuti Iye sakumva. 3Pakuti manja anu
adetsedwa ndi mwazi, ndi zala zanu ndi mphulupulu, milomo yanu
yanena zonama, lilime lanu lilankhula moipa. 4Palibe woturutsa
mlandu molungama, ndipo palibe wonena zoona; iwo akhulupirira
mwacabe, nanena zonama; iwo atenga kusayeruzika ndi kubala
mphulupulu, 5Iwo afungatira mazira a mamba aswetse, naluka
ukonde wa tandaude; iye amene adya mazira ace amafa, ndi
coswanyikaco cisweka nicikhala songo. 6Maukonde ao sadzakhala
zobvala, sadzapfunda nchito zao; nchito zao ziri nchito zoipa, ndi
ciwawa ciri m'manja mwao. 7Mapazi ao athamangira koipa, ndipo
iwo afulumira kukhetsa mwazi wosacimwa; maganizo ao ali
maganizo oipa; bwinja ndi cipasuko ziri m'njira mwao. 8Njira ya
mtendere saidziwa, ndipo palibe ciweruziro m'mayendedwe mwao;
akhotetsa njira zao; ali yense ayenda m'menemo sadziwa
mtendere. 9Cifukwa cace ciweruziro ciri patari ndi ife, ndi
cilungamo sicitipeza; tiyang'anira kuunika, koma taona mdima;
tiyang'anira kuyera, koma tiyenda m'usiku. 10Tiyambasira khoma
ngati wakhungu, inde tiyambasa monga iwo opanda maso;
tipunthwa usana monga m'cizirezire; tiri m'malo amdima ngati
akufa. 11Tonse tibangula ngati zirombo, ndi kulira maliro zolimba
ngati nkhunda; tiyang'anira ciweruziro koma palibe; tiyang'anira
cipulumutso koma ciri patari ndi ife. 12Pakuti zolakwa zathu
zacuruka pamaso pa Inu, ndipo macimo athu atineneza ife; pakuti
zolakwa zathu ziri ndi ife, ndipo zoipa zathu tizidziwa; 13ndizo
kulakwabe ndi kukanabe Yehova, ndi kuleka kutsata Mulungu
wathu, kulankhula zotsendereza ndi kupanduka, kuganizira ndi
kunena pakamwa mau akunyenga oturuka mumtima. 14Ndipo
ciweruziro cabwerera m'mbuyo, ndi cilungamo caima patari; pakuti
coona cagwa m'khwalala, ndi kuongoka sikungalowe. 15Inde coona
cisoweka; iye amene asiya coipa, zifunkhidwa zace; ndipo Yehova
anaona ici, ndipo cidamuipira kuti palibe ciweruzo. 16Ndipo Iye
anaona kuti palibe munthu, nazizwa kuti palibe wopembedzera;
cifukwa cace mkono wace wace unadzitengera yekha cipulumutso;
ndi cilungamo cace cinamcirikiza. 17Ndipo anabvala cilungamo
monga cida ca pacifuwa, ndi cisoti ca cipulumutso pamutu pace;
nabvala zobvala zakubwezera cilango, nabvekedwa ndi cangu
monga copfunda, 18Monga mwa nchito zao momwemo Iye
adzabwezera amaliwongo ace ukali, nadzabwezera adani ace

cilango; nadzabwezeranso zisumbu cilango. 19Comweco iwo
adzaopa dzina la Yehova kucokera kumadzulo, ndi ulemerero wace
kumene kuturukira dzuwa; pakuti pamene mdani adzafika ngati
cigumula, mzimu wa Yehova udzamkwezera mbendera
yomletsa. 20Ndipo Mombolo adzafika ku Ziyoni, ndi kwa iwo amene
atembenuka kusiya kulakwa mwa Yakobo, ati Yehova. 21Ndipo
kunena za. Ine, ili ndi pangano langa ndi iwo, ati Yehova; mzimu
wanga umene uli pa iwe, ndi mau anga amene ndaika m'kamwa
mwako sadzacoka m'kamwa mwako, pena m'kamwa mwa ana ako,
pena m'kamwa mwa mbeu ya mbeu yako, ati Yehova, kuyambira
tsopano ndi ku nthawi zonse.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Ulemerero wa Yerusalemu ubwezedwa

1Nyamuka, wala, pakuti kuunika kwake kwafika, ndi ulemerero wa
Yehova wakuturukira. 2Pakuti taona, mdima udzaphimba dziko
lapansi, ndi mdima wa bii mitundu ya anthu; koma Yehova
adzakuturukira, ndi ulemerero wace udzaoneka pa iwe. 3Ndipo
amitundu adzafika kwa kuunika kwako, ndi mafumu kwa kuyera
kwa kuturuka kwake, 4Tukula maso ako uunguze-unguze ndi kuona;
iwo onse asonkhana pamodzi, adza kwa iwe; ana ako amuna
adzacokera kutari, ndi ana ako akazi adzaleredwa
pambali. 5Pamenepo udzaona ndi kuunikidwa, ndipo mtima wako
udzanthunthumira ndi kukuzidwa; pakuti unyinji wa nyanja
udzakutembenukira, cuma ca amitundu cidzafika kwa iwe. 6Gulu la
ngamila lidzakukuta, ngamila zazing'ono za Midyani ndi Efa; iwo
onsewo adzacokera ku Seba adzabwera nazo golidi ndi zonunkhira;
ndipo adzalalikira matamando a Yehova. 7Zoweta za Kedara
zidzasonkhana kwa iwe, nkhosa zamphongo za Nebaioti
zidzakutumikira; izo zidzafika ndi kulandiridwa pa guwa langa la
nsembe; ndipo ndidzakometsa nyumba ya ulemerero
wanga. 8Ndani awa amene auluka ngati mtambo, ndi monga
nkhunda ku mazenera ao? 9Zoonadi, zisumbu zidzandilindira Ine;
zidzayamba ndi ngalawa za Tarisi kutenga ana ako amuna kutari,
golidi wao ndi siliva wao pamodzi nao, cifukwa ca dzina la Yehova
Mulungu wako, ndi cifukwa ca Woyera wa Israyeli, popeza Iye
wakukometsa iwe. 10Ndipo alendo adzamanga malinga ako, ndi
mafumu ao adzakutumikira; pakuti m'kukwiya kwanga
ndinakantha, koma mokomera mtima ndidakucitira iwe
cifundo. 11Zipata zako zidzakhalabe zotseguka, sizidzatsekedwa
usana pena usiku, kuti abwere naco kwa iwe cuma ca amitundu,
ndi mafumu ao otsogozedwa nao pamodzi. 12Pakuti mtundu ndi
ufumu umene udzakana kukutumikira udzaonongeka; inde
mitundu imeneyo idzasakazidwa ndithu. 13Ulemerero wa Lebano
udzafika kwa iwe; mtengo wamlombwa, mtengo wamkuyu ndi
mtengo wanaphini pamodzi, kukometsera malo a kacisi wanga;
ndipo ndidzacititsa malo a mapazi anga ulemerero. 14Ndipo ana
amuna a iwo amene anabvuta iwe adzafika, nadzakugwadira;
ndipo iwo onse amene anakucepetsa iwe adzagwadira ku mapazi
ako, nadzakucha iwe, Mudzi wa Yehova, Ziyoni wa Woyera wa
Israyeli. 15Ungakhale unasiyidwa ndi kudedwa, osapita munthu
mwa iwe, Ine ndidzakusandutsa cangwiro cosatha, cokondweretsa
ca mibadwo yambiri. 16Iwe udzayamwanso mkaka wa amitundu,
nudzayamwa bere la mafumu, nudzadziwa kuti Ine Yehova ndine
mpulumutsi wako, ndi Mombolo wako, Wamphamvu wa

Yakobo. 17M'malo mwa mkuwa ndidzatenga golidi, ndi m'malo mwa
citsulo ndidzatenga siliva, ndi m'malo mwa mtengo ndidzatenga
mkuwa, ndi m'malo mwa miyala ndidzatenga citsulo; ndidzakuikira
akapitao a mtendere, ndi oyang'anira nchito a
cilungamo. 18Ciwawa sicidzamvekanso m'dziko mwako,
kupululutsa pena kupasula m'malire ako; koma udzacha malinga
ako Cipulumutso, ndi zipata zako Matamando. 19Dzuwa
silidzakhalanso kuunika kwako usana, ngakhale mwezi
sudzakuunikiranso kuti kuyere; koma Yehova adzakhala kwa iwe
kuunika kosatha, ndi Mulungu wako adzakhala ulemerero
wako. 20Dzuwa lako silidzalowanso, mwezi wako sudzanka
kumidima; pakuti Yehova adzakhala kuunika kwako kosatha, ndi
masiku a kulira maliro ako adzatha. 21Anthu ako adzakhalanso
onse olungama; dzikolo lidzakhala colowa cao ku nthawi zonse,
nthambi yooka Ine, nchito ya manja anga, kuti Ine
ndikuzidwe. 22Wamng'ono adzasanduka cikwi, ndi wocepa
adzasanduka mtundu wamphamvu; Ine Yehova ndidzafulumiza ici
m'nthawi yace.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Alalikira Uthenga Wabwino wa cipulumutso

1Mzimu wa Ambuye Yehova uli pa ine; pakuti Yehova wandidzoza
ine ndilalikire mau abwino kwa ofatsa; Iye wanditumiza
ndikamange osweka mtima, ndikalalikire kwa am'nsinga
mamasulidwe, ndi kwa omangidwakutsegulidwa kwa
m'ndende; 2ndikalalikire caka cokomera Yehova, ndi tsiku
lakubwezera la Mulungu wathu; ndikatonthoze mtima wa onse
amene akulira maliro; 3ndikakonzere iwo amene alira maliro
m'Ziyoni, ndi kuwapatsa cobvala kokometsa m'malo mwa phulusa,
mafuta akukondwa m'malo mwa maliro, cobvala ca matamando
m'malo mwa mzimu wopsinjika; kuti iwo achedwe mitengo ya
cilungamo yakuioka Yehova, kuti Iye alemekezedwe. 4Ndipo iwo
adzamanga mabwinja akale, nadzamanga pa miunda yakale,
nadzakonzanso midzi yopasuka, mabwinja a mibadwo
yambiri. 5Ndipo alendo adzaimirira ndi kudyetsa magulu ako, ndi
anthu akunja adzakhala olima ako, ndi kukukonzera minda
yamphesa. 6Koma inu mudzachedwa ansembe a Yehova; anthu
adzakuyesani inu atumiki a Mulungu wathu; inu mudzadya cuma
ca amitundu, nimudzalowa mu ulemerero wao. 7M'malo mwa
manyazi anu, owirikiza; ndi citonzo iwo adzakondwera ndi gawo
lao; cifukwa cace iwo adzakhala naco m'dziko mwao colowa
cowirikiza, adzakhala naco cikondwerero cosatha. 8Pakuti Ine
Yehova ndikonda ciweruziro, ndida cifwamba ndi coipa; ndipo
ndidzawapatsa mphotho yao m'zoonadi; ndipo ndidzapangana nao
pangano losatha. 9Ndipo ana ao adzadziwidwa mwa amitundu, ndi
obadwa ao mwa anthu; onse amene awaona adzawazindikira kuti
iwo ndiwo ana amene Yehova wadalitsa.
10Ndidzakondwa kwambiri mwa Yehova, moyo wanga
udzakondwerera mwa Mulungu wanga; pakuti Iye wandibveka ine
ndi zobvala za cipulumutso, nandipfunda copfunda ca cilungamo,
monga mkwati abvala nduwira, ndi monga mkwatibwi adzikometsa
yekha ndi miyala yamtengo. 11Pakuti monga dziko liphukitsa
mphundu zace, ndi monga munda umeretsa zobzalamo,
momwemo Ambuye Yehova adzaphukitsa cilungamo ndi
matamando pamaso pa amitundu onse.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Cikhalidwe cokoma ca Yerusalemu

1Cifukwa ca Ziyoni sindidzakhala cete, ndi cifukwa ca Yerusalemu
sindidzapuma, kufikira cilungamo cace cidzaturuka monga kuyera,
ndi cipulumutso cace monga nyali yoyaka. 2Ndipo amitundu
adzaona cilungamo cako, ndi mafumu onse ulemerero wako; ndipo
udzachedwa dzina latsopano, limene m'kamwa mwa Yehova
mudzachula. 3Iwe udzakhalanso korona wokongola m'dzanja la
Yehova, korona wacifumu m'dzanja la Mulungu wako. 4Iwe
sudzachedwanso Wosiyidwa; dziko lako silidzachedwanso Bwinja;
koma iwe udzachedwa Hefiziba ndi dziko lako Beula; pakuti Yehova
akondwera mwa iwe, ndipo dziko lako lidzakwatiwa. 5Pakuti monga
mnyamata akwatira namwali, momwemo ana ako amuna
adzakukwama iwe; ndi monga mkwati akondwera ndi mkwatibwi,
momwemo Mulungu wako adzakondwera nawe.
6Ndaika alonda pa malinga ako, Yerusalemu; iwo sadzakhala cete
usana pena usiku; inu akukumbutsa Yehova musakhale
cete, 7ndipo musamlole akhale cete, kufikira Iye atakhazikitsa
naika Yerusalemu akhale tamando m'dziko lapansi. 8Yehova
analumbira pa dzanja lace lamanja, ndi mkono wace wamphamvu,
Zoonadi, sindidzaperekanso tirigu wako akhale cakudya ca adani
ako, ndipo alendo sadzamwa vinyo wako amene iwe unagwirira
nchito; 9koma iwo amene adzakolola adzadya ndi kutamanda
Yehova; ndi iwo amene adzamchera adzamumwa m'mabwalo a
kacisi wanga.
10Pitani, pitani pazipata; konzani njira ya anthu; undani, undani
khwalala; cotsani miyala, kwezani mbendera ya anthu. 11Taonani,
Yehova walalikira kufikira malekezero a dziko lapansi. Nenani kwa
mwana wamkazi wa Ziyoni, Taona cipulumutso cako cifika; taona
mphotho yace ali nayo, ndi nchito yace iri pamaso pace. 12Ndipo
iwo adzawacha Anthu opatulika, Oomboledwa a Yehova; ndipo iwe
udzachedwa Wofunidwa, Mudzi wosasiyidwa.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Mulungu adzapulumutsa anthu ace, nadzabwezera cilango owasautsa

1Ndani uyu alinkudza kucokera ku Edomu, ndi zobvala zonika
zocokera ku Bozira? uyu wolemekezeka m'cobvala cace, nayenda
mu ukuru wa mphamvu zace? Ndine amene ndilankhula
m'colungama, wa mphamvu yakupulumutsa, 2Cophimba cako
cifiiriranji, ndi zobvala zako zifanana bwanji ndi woponda
mopondera mphesa? 3Ndaponda ndekha mopondera mphesa,
ndipo panalibe nane mmodzi wa mitundu ya anthu; inde
ndinawaponda m'kukwiya kwanga, ndi kuwapondereza mu ukali
wanga: ndi mwazi wa moyo wao unawazidwa pa zobvala zanga;
ndipo ndadetsa copfunda canga conse. 4Pakuti tsiku lakubwezera
liri mumtima mwanga, ndi caka ca kuombola anthu anga
cafika. 5Ndipo ndinayang'ana, koma panalibe wothangata; ndipo
ndinadabwa kuti panalibe wocirikiza; cifukwa cace mkono wanga
wanga unanditengera cipulumutso, ndi ukali wanga unandicirikiza
Ine. 6Ndipo ndinapondereza anthu m'kukwiya kwanga, ndi
kuwatswanya mu ukali wanga, ndi kutsanulira mwazi wa moyo
wao.

Kuyamika, kuulula zoipa, ndi kupempha kwa anthu a Mulungu

7Ndidzachula za cifundo cace ca Yehova, ndi matamando a Yehova,
monga mwa zonse zimene Yehova wapereka kwa ife; ndi ubwino
wace waukuru kwa banja la Israyeli, umene Iye wapereka kwa iwo,
monga mwa cifundo cace, ndi monga mwa nchito zocuruka za
cikondi cace. 8Pakuti anati, Zoonadi iwo ndiwo anthu anga, ana
amene sangacite monyenga; comweco Iye anali Mpulumutsi
wao. 9M'mazunzo ao onse Iye anazunzidwa, ndipo mthenga
wakuimirira pamaso pace anawapulumutsa; m'kukonda kwace ndi
m'cisoni cace Iye anawaombola, nawabereka nawanyamula masiku
onse akale. 10Koma iwo anapandukira ndi kumvetsa cisoni mzimu
wace woyera, cifukwa cace Iye anasandulika mdani wao,
nawathira nkhondo Iye yekha. 11Pamenepo iwo anakumbukira
masiku akale, Mose ndi anthu ace, nati, Ali kuti Iye amene
anawaturutsa m'nyanja pamodzi ndi abusa a gulu lace? Ali kuti Iye
amene anaika mzimu wace woyera pakati pao, 12amene
anayendetsa mkono wace waulemerero pa dzanja lamanja la
Mose? amene anagawanitsa madzi pamaso pao, kuti adzitengere
mbiri yosatha? 13amene anawatsogolera kupitira mwa kuya monga
kavalo m'cipululu osapunthwa iwo? 14Monga ng'ombe zotsikira
kucigwa mzimu wa Yehova unawapumitsa; comweco inu

munatsogolera anthu anu kudzitengera mbiri
yaulemerero. 15Tayang'anani kunsi, taonani pokhala panu poyera,
ndi pa ulemerero wanu, cangu canu ndi nchito zanu zamphamvu
ziri kuti? mwanditsekerezera zofunafuna za mtima wanu ndi cisoni
canu. 16Pakuti Inu ndinu Atate wathu, ngakhale Abrahamu
satidziwa ife, ndi Israyeli satizindikira ife. Inu Yehova ndinu Atate
wathu, Mombolo wathu wacikhalire ndi dzina lanu. 17Yehova bwanji
mwatisoceretsa kusiya njira zanu, ndi kuumitsa mitima yathu
tisakuopeni? Bwerani, cifukwa ca atumiki anu, mafuko a colowa
canu. 18Anthu anu opatulika anakhala naco kanthawi kokha; adani
athu apondereza kacisi wanu wopatulika. 19Ife takhala ngati iwo
amene simunawalamulira konse, ngati iwo amene sanachedwa
dzina lanu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Yesaya 64

1Mwenzi mutang'amba kumwamba ndi kutsikira pansi, kuti mapiri
agwedezeke pamaso panu; 2monga pamene moto uyatsa zitsamba,
ndi moto uwiritsa madzi; kudziwitsa kwa amaliwongo anu dzina
lanu, kuti amitundu anthunthumire pamaso panu, 3Pamene Inu
munacita zinthu zoopsya, zimene ife sitinayang'anira, Inu
munatsika, mapiri anagwedezeka pamaso panu. 4Pakuti kuyambira
kale anthu sanamve pena kumvetsa ndi khutu, ngakhale diso
silinaone Mulungu wina popanda Inu, amene amgwirira nchito iye
amene amlindirira Iye. 5Inu mukomana ndi iye amene akondwerera,
nacita cilungamo, iwo amene akumbukira Inu m'njira zanu; taonani
Inu munakwiya, ndipo ife tinacimwa; takhala momwemo nthawi
yambiri, kodi tidzapulumutsidwa? 6Pakuti ife tonse takhala ngati
wina amene ali wosakonzeka; ndi zolungama zathu zonse ziri ngati
cobvala codetsedwa; ndipo ife tonse tifota monga tsamba, ndi zoipa
zathu zitiuluza monga mphepo. 7Ndipo palibe amene aitana dzina
lanu, amene adzikangamiza yekha kugwiritsa Inu; pakuti Inu
mwatibisira nkhope yanu, ndipo mwatinyeketsa ndi zoipa
zathu. 8Koma tsopano, Yehova, Inu ndinu Atate wathu; ife tiri dongo,
ndipo Inu ndinu Muumbi wathu; ndipo ife tonse tiri nchito ya dzanja
lanu. 9Musakwiye kopambana, Yehova, musakumbukire zoipa
nthawi zonse; taonani, yang'anani ife, tikupembedzani Inu, ife tonse
tiri anthu anu. 10Midzi yanu yopatulika yasanduka cipululu, Ziyoni
wasanduka cipululu, Yerusalemu wasanduka bwinja. 11Nyumba
yathu yopatulika ndi yokongola, m'mene makolo athu
anakutamandani Inu, yatenthedwa ndi moto; ndi zinthu zathu zonse
zokondweretsa zapasuka. 12Kodi mudzadziletsa pa zinthuzi, Yehova?
Kodi Inu mudzakhala cete ndi kutibvutitsa ife zolimba?

©The Bible Society of Malawi, 1992

Acenjeza osamvera kuti adzalangidwa

1Iwo amene sanafunsa za Ine andifunafuna; ndi iwo amene
sanandipwaira andipeza; ndinati, Taonani Ine, taonani Ine, kwa
mtundu umene sunachula dzina langa. 2Ndatambasulira manja
anga tsiku lonse kwa anthu opanduka, amene ayenda m'njira
mosati mwabwino, kutsata maganizo ao ao; 3anthu amene
andiputa Ine kumaso kwanga nthawi zonse, apereka nsembe
m'minda, nafukizira zonunkhira panjerwa; 4amene akhala pakati
pa manda, ndi kugona m'malo am'tseri; amene adya nyama ya
nkhumba, ndi msuzi wa zinthu zonyansa uli m'mbale zao; 5amene
ati, Ima pa wekha, usadze cifupi ndi ine, pakuti ine ndiri woyera
kupambana iwe; amenewa ndiwo utsi m'mphuno mwanga, moto
woyaka tsiku lonse. 6Taonani, calembedwa pamaso panga;
sindidzakhala cete, koma ndidzabwezera, inde ndidzabwezera pa
cifuwa cao, 7zoipa zanu zanu pamodzi ndi zoipa za makolo anu, ati
Yehova, amene anafukiza zonunkhira pamapiri, nandicitira mwano
pazitunda; cifukwa cace Ine ndidzayesa nchito yao yakale ilowe pa
cifuwa cao.
8Atero Yehova, Monga vinyo watsopano apezedwa m'tsango, ndipo
wina ati, Usalitsononge, pakuti muli mdalitso m'menemo, momwemo
ndidzacita cifukwa ca atumiki anga, kuti ndisawaononge
onse. 9Ndipo ndidzaturutsa mbeu mwa Yakobo, ndi mwa Yuda
wolowa nyumba wa mapiri anga; ndipo osankhidwa anga
adzalandira colowa cao, ndi atumiki anga adzakhala
kumeneko. 10Ndipo Saroni adzakhala podyetsera nkhosa, ndi cigwa
ca Akori cidzakhala pogona zoweta kwa anthu anga amene
andifuna Ine. 11Koma inu amene mwasiya Yehova, amene
mwaiwala phiri langa lopatulika, ndi kukonzera mlungu wamwai
gome, ndi kudzazira mlungu waimfa zikho za vinyo
wosanganiza; 12ndidzasankhiratu inu kulupanga, ndipo inu nonse
mudzagwada ndi kuphedwa; pakuti pamene ndinaitana, inu
simunayankhe; pamene ndinanena, simunamve; koma munacita
coipa m'maso mwanga, ndi kusankha cimene Ine sindinakondwera
naco.
13Cifukwa cace atero Ambuye Yehova, Taonani atumiki anga
adzadya, koma inu mudzakhala ndi njala; taonani, atumiki anga
adzamwa, koma inu mudzakhala ndi ludzu; taonani, atumiki anga
adzasangalala, koma inu mudzakhala ndi manyazi; 14taonani,
atumiki anga adzayimba ndi mtima wosangalala, koma inu
mudzalira ndi mtima wacisoni; ndipo mudzapfuula cifukwa ca
kusweka mzimu. 15Ndipo mudzasiya dzina lanu likhale citemberero
kwa osankhidwa anga, ndipo Ambuye Yehova adzakupha iwe,

nadzacha atumiki ace dzina lina; 16comweco iye amene adzidalitsa
yekha m'dziko lapansi, adzadzidalitsa yekha mwa Mulungu woona;
ndipo iye amene alumbira m'dziko lapansi adzalumbira pa
Mulungu woona; popeza zobvuta zoyamba zaiwalika, ndi popeza
zabisalika kumaso kwanga.

Kumwamba kwatsopano ndi dziko lapansi latsopano

17Pakuti taonani, ndilenga kumwamba kwa tsopano ndi dziko
lapansi latsopano; ndipo zinthu zakale sizidzakumbukika, pena
kulowa mumtima. 18Koma khalani inu okondwa ndi kusangalala ku
nthawi zonse ndi ici ndicilenga; pakuti taonani, ndilenga
Yerusalemu wosangalala, ndi anthu ace okondwa. 19Ndipo
ndidzasangalala m'Yerusalemu, ndi kukondwera mwa anthu anga;
ndipo mau akulira sadzamvekanso mwa iye, pena mau
akupfuula. 20Sipadzakhalanso khanda la masiku, pena munthu
wokalamba osakwanitsa masiku ace; pakuti mwana adzafa wa
zaka zana limodzi; ndipo wocimwa pokhala wa zaka zana limodzi
adzatembereredwa. 21Ndipo iwo adzamanga nyumba ndi
kukhalamo; ndipo iwo adzanka minda yamphesa, ndi kudya zipatso
zace. 22Iwo sadzamanga, ndi wina kukhalamo; iwo sadzanka, ndi
wina kudya; pakuti monga masiku a mtengo adzakhalamasiku a
anthu anga; ndi osankhidwa anga adzasangalala nthawi zambiri
ndi nchito za manja ao. 23Iwo sadzagwira nchito mwacabe, pena
kubalira tsoka; pakuti iwo ndiwo mbeu ya odalitsidwa a Yehova, ndi
obadwa ao adzakhala pamodzi ndi iwo. 24Ndipo padzakhala kuti
iwo asanaitane Ine, ndidzayankha; ndipo ali cilankhulire, Ine
ndidzamva. 25Mmbulu ndi mwana wa nkhosa zidzadyera pamodzi;
ndi mkango udzadya udzu ngati ng'ombe; ndi pfumbi lidzakhala
cakudya ca njoka; sizidzapwetekana, kapena kusakazana m'phiri
langa lonse lopatulika, ati Yehova.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Ocita zoipa adzabwezedwa cilango

1Atero Yehova, Kumwamba ndi mpando wanga wacifumu, ndi dziko
lapansi ndi coikapo mapazi anga; mudzandimangira Ine nyumba
yotani? ndi malo ondiyenera kupumamo ali kuti? 2Pakuti zonsezi
mkono wanga wazilenga, momwemo zonsezi zinaoneka, ati
Yehova; koma ndidzayang'anira munthu uyu amene ali
waumphawi, ndi wa mzimu wosweka, nanthunthumira ndi mau
anga. 3Wakupha ng'ombe alingana ndi wakupha munthu; iye
wapereka nsembe ya mwana wa nkhosa alingana ndi wotyola
khosi la garu; wothira nsembe yaufa akunga wothira mwazi wa
nkhumba; wofukiza conunkhira akunga wodalitsa fano; inde iwo
asankha njira zao zao, ndipo moyo wao ukondwerera m'zonyansa
zao; 4Inenso ndidzasankha zodzinyenga nazo, ndipo ndidzatengera
mantha ao pa iwo; pakuti pamene ndinaitana, panalibe woyankha;
pamene ndinalankhula, iwo sanamva konse; koma anacita coipa
m'maso mwanga, ndi kusankha cimene ndisanakondwere naco.
5Imvani mau a Yehova, inu amene munthunthumira ndi mau ace;
abale anu amene akudani inu, amene anaponya inu kunja cifukwa
ca dzina langa, iwo anati, Yehova alemekezedwe, kuti ife tione
kusangalala kwanu; koma iwo adzakhala ndi manyazi. 6Mau a
phokoso acokera m'mudzi, mau ocokera m'Kacisi, mau a Yehova
amene abwezera adani ace cilango. 7Mkazi asanamve zowawa,
anabala mwana; kupweteka kwace kusanadze, anabala mwana
wamwamuna. 8Ndani anamva kanthu kotereko? ndani anaona
zinthu zoterezo? Kodi dziko lidzabadwa tsiku limodzi? Kodi mtundu
udzabadwa modzidzimutsa? pakuti pamene Ziyoni anamva
zowawa, pomwepo anabala ana ace. 9Kodi Ine ndidzafikitsira mkazi
nthawi yakutula osamtulitsa? ati Yehova; kodi Ine amene ndibalitsa
ndidzatseka mimba? ati Mulungu wako.

Yehova adzaweruza omcimwira

10Sangalalani inu pamodzi ndi Yerusalemu, ndipo kondwani cifukwa
ca iye, inu nonse amene mumkonda; sangalalani kokondwa
pamodzi ndi iye, inu nonse akumlira maliro; 11kuti mukayamwe ndi
kukhuta ndi mabere a zitonthozo zace; kuti mukafinye mkaka ndi
kukondwerera ndi unyinji wa ulemerero wace. 12Pakuti atero
Yehova, Taonani ndidzamfikitsira mtendere ngati mtsinje, ndi
ulemerero wa amitundu ngati mtsinje wosefukira. Inu
mudzayamwa, ndi kunyamulidwa pambali, ndi kululuzidwa pa
maondo, 13Monga munthu amene amace amtonthoza mtima,
momwemo ndidzatonthoza mtima wanu; ndipo mudzatonthozedwa
mtima m'Yerusalemu. 14Ndipo mudzaciona, ndipo mtima wanu
udzasangalala, ndipo mafupa anu adzakula ngati msipu; ndipo

dzanja la Yehova lidzadziwika ndi atumiki ace, ndipo adzakwiyira adani ace. 15Pakuti taonani, Yehova adzafika m'moto, ndi magareta ace adzafanana ndi kabvumvulu; kubwezera mkwiyo wace ndi ukali, ndi kudzudzula ndi malawi amoto, 16Pakuti Yehova adzatsutsana ndi moto, ndi lupanga lace, ndi anthu onse; ndi ophedwa a Yehova adzakhala ambiri. 17Iwo amene adzipatulitsa nadziyeretsa, kuti amuke kuminda tsatane tsatane, ndi kudya nyama ya nkhumba, ndi conyansa, ndi mbewa, adzathedwa pamodzi, ati Yehova. 18Pakuti Ine ndidziwa nchito zao ndi maganizo ao; nthawi ikudza yakudzasonkhanitsa Ine a mitundu yonse ndi zinenedwe zonse, ndipo adzafika nadzaona ulemerero wanga. 19Ndipo ndidzaika cizindikiro pakati pao, ndipo ndidzatumiza onse amene apulumuka mwa iwo kwa amitundu, kwa Tarisi, kwa Puli ndi kwa Aludi, okoka uta kwa Tubali ndi Yavana, ku zisumbu zakutari, amene sanamve mbiri yanga, ngakhale kuona ulemerero wanga; ndipo adzabukitsa ulemerero wanga pakati pa amitundu. 20Ndipo iwo adzatenga abale anu onse mwa amitundu onse akhale nsembe ya kwa Yehova; adzabwera nao pa akavalo, ndi m'magareta, ndi m'macila, ndi pa nyuru, ndi pa ngamila, kudza ku phiri langa lopatulika ku Yerusalemu, ati Yehova, monga ana a Israyeli abwera nazo nsembe zao m'cotengera cokonzeka ku nyumba ya Yehova. 21Ndipo ena a iwo ndidzawatenga akhale ansembe ndi Alevi, ati Yehova. 22Pakuti monga m'mwamba mwatsopano ndi dziko lapansi latsopano limene ndidzalenga, lidzakhalabe pamaso pa Ine, ati Yehova, momwemo adzakhalabe ana anu ndi dzina lanu. 23Ndipo kudzakhala kuti kuyambira pa mwezi wokhala kufikira ku unzace, ndi kuyambira pa Sabata lina kufikira ku linzace, anthu onse adzafika kudzapembedzera pamaso pa Ine, ati Yehova. 24Ndipo iwo adzaturuka ndi kuyang'ana mitembo ya anthu amene andilakwira Ine, pakuti mbozi yao sidzafa, pena moto wao sudzazimidwa; ndipo iwo adzanyansa anthu onse.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Jeremiah

Yeremiya 1

Kuitanidwa kwa Yeremiya akhale mneneri

1MAU a Yeremiya mwana wa Hilikiya, wa ansembe amene anali ku Anatoti
m'dziko la Benjamini; 2amene anamdzera mau a Yehova masiku a Yosiya
mwana wace wa Amoni, mfumu ya Ayuda caka cakhumi ndi citatu ca ufumu
wace. 3Anamdzeranso masiku a Yehoyakimu mwana wace wa Yosiya, mfumu
ya Yuda, kufikira Zedekiya mwana wace wa Yosiya mfumu ya Yuda atatsiriza
zaka khumi ndi cimodzi; kufikira a ku Yerusalemu anatengedwa ndende mwezi
wacisanu.
4Ndipo anadza kwa ine mau a Yehova, kuti, 5Ndisanakulenge iwe m'mimba
ndinakudziwa, ndipo usanabadwe ndinakupatula iwe; ndinakuika kuti ukhale
mneneri wa mitundu ya anthu. 6Ndipo ndinati, Ha, Ambuye Mulungu! taonani,
sindithai kunena pakuti ndiri mwana. 7Koma Yehova anati kwa ine, Usati,
ndine mwana pakuti udzanka kwa yense amene ndidzakutumako iwe,
nudzanena conse cimene ndidzakuuza. 8Usaope nkhope zao; cifukwa Ine ndiri
ndi iwe kuti ndikulanditse iwe, ati Yehova. 9Ndipo Yehova anaturutsa dzanja
lace, na'khudza pakamwa panga; nati Yehova kwa ine, Taona ndaika mau
anga m'kamwa mwako; 10penyatu, lero ndakuika ulamulire mitundu ya anthu
ndi maufumu, kuti uzule, upasule, uononge, ugwetse; umange, ubzyale.

Masomphenya oyamba a Yeremiya

11Ndipo mau a Yehova anadza kwa ine, kuti, Yeremiya, uona ciani? Ndipo
ndinati, Ine ndiona ntyole ya katungurume. 12Ndipo Yehova anati kwa ine,
Waona bwino pakuti Ine ndidzadikira mau anga kuwacita. 13Ndipo mau a
Yehova anadza kwa ine nthawi yaciwiri, kuti, ona ciani? Ndipo ndinati, Ine
ndiona mphika wogaduka; ndi pakamwa pace unafulatira kumpoto. 14Ndipo
Yehova anati kwa ine, Kucokera kumpoto coipa cidzaturukira onse okhala
m'dziko. 15Pakuti, taona, ndidzaitana mabanja onse a maufumu a kumpoto,
ati Yehova; ndipo adzafika nadzaika yense mpando wacifumu wace pa zipata
za Yerusalemu, ndi pa malinga onse ozinga pamenepo, ndi pa midzi yonse ya
Yuda. 16Ndipo ndidzanena nao za maweruzo anga akuweruzira zoipa zao
zonse; popeza anandisiya Ine, nafukizira milungu yina, nagwadira nchito za
manja ao. 17Koma iwe ukwinde m'cuuno mwako, nuuke, nunene kwa iwo
zonse zimene ndikuuza iwe; usaope nkhope zao ndingakuopetse iwe pamaso
pao. 18Cifukwa, taona, ndakuyesa iwe lero mudzi walinga, mzati wacitsulo,
makoma amkuwa, pa dziko lonse, ndi pa mafumu a Yuda, ndi pa akuru ace,
ndi pa ansembe ace, ndi pa anthu a m'dziko. 19Ndipo adzamenyana ndi iwe;
koma sadzakuposa; cifukwa Ine ndiri ndi iwe, ati Yehova, kukulanditsa.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Yehova adzudzula anthu a Israyeli

1Ndipo mau a Yehova anadza kwa ine, nati, 2Pita nupfuule
n'makutu a Yerusalemu, kuti, Yehova atero, Ndikumbukira za iwe
kukoma mtima kwa ubwana wako, cikondi ca matomedwe ako;
muja unanditsata m'cipululu m'dziko losabzya lamo. 3Israyeli anali
wopatulikira Yehova, zipatso zoundukula za zopindula zace; onse
amene adzamudya iye adzayesedwa oparamula; coipa
cidzawagwera, ati Yehova.
4Tamvani mau a Yehova, iwe nyumba ya Yakobo, ndi inu mabanja
onse a nyumba ya Israyeli; 5atero Yehova, Atate anu apeza
cosalungama canji mwa Ine, kuti andicokera kunka kutari, natsata
zacabe, nasanduka acabe? 6Osati, Ali kuti Yehova amene
anatikweza kucokera ku dziko la Aigupto, natitsogolera m'cipululu,
m'dziko loti se ndi la maenje, m'dziko la cirala ndi la mthunzi wa
imfa, m'dziko losapitamo anthu, losamangamo anthu? 7Ndipo
ndinakulowetsani m'dziko la minda, kuti mudye zipatso zace, ndi
zabwino zace; koma pamene munalowa, munaipitsa dziko langa,
ndi kuyesa colandira canga conyansa. 8Ansembe sanati, Ali kuti
Yehova? ndi iwo amene agwira malamulo sandidziwa Ine; ndi
abusa omwe anandilakwira Ine, ndi aneneri ananenera mwa Baala,
natsata zinthu zosapindula. 9Cifukwa cace ndidzatsutsananso
nanu, ati Yehova, ndi ana a ana anu ndidzatsutsana nao. 10Pakuti
pitani ku zisumbu za Kitimu nimuone; tumizani ku Kedara
nimulingalire bwino; nimuone ngati cinalipo cotere. 11Kodi mtundu
wa anthu unasintha milungu yao, imene siiri milungu? Koma anthu
anga anasintha ulemerero wao ndi cosapindula. 12Muzizwe
pamenepo, miyamba inu, muope kwambiri, mukhale ouma, ati
Yehova. 13Pakuti anthu anga anacita zoipa ziwiri; anandisiya Ine
kasupe wa madzi amoyo, nadziboolera zitsime, zitsime zong'aluka,
zosakhalamo madzi. 14Kodi Israyeli ndi mtumiki? kodi ndiye kapolo
wobadwa m'nyumba? afunkhidwa bwanji? 15Ana a mikango
anambangulira iye, nakweza mau; anapasula dziko lace, midzi
yace yatenthedwa, mulibenso wokhalamo. 16Ananso a Nofi ndi a
Tahapanesi, anaswa pakati pamtu pako. 17Kodi sunadzicitira ici iwe
wekha popeza unasiya Yehova Mulungu wako, pamene
anatsogolera iwe panjira? 18Tsopano uli naco ciani m'njira ya ku
Aigupto, kumwa madzi a Sihori? uli naco ciani m'njira ya ku Asuri,
kumwa madzi a m'Nyanja? 19Coipa cako cidzai kulanga iwe,
mabwerero ako adzakudzudzula iwe; dziwa, nuone, kuti ici ndi
coipa ndi cowawa, kuti wasiya Yehova Mulungu wako, ndi kuti
kundiopa Ine sikuli mwa iwe, ati Yehova Mulungu wa
makamu. 20Pakuti kale lomwe ndinatyola gori lako, ndi kudula
zomangira zako; ndipo unati, Sindidzakutumikirani, pakuti pa

zitunda zonse zazitari, ndi patsinde pa mitengo yonse yaiwisi
unawerama, ndi kucita dama. 21Ndipo Ine ndinakuoka mpesa
wangwiro, mbeu yoona; kodi bwanji wandisandukira Ine mbeu
yopanda pace, ya mpesa wacilendo? 22Pakuti ngakhale usamba ndi
soda, ndi kudzitengera sopo wambiri, mphulupulu zako zidziwika
pamaso panga, ati Yehova Mulungu. 23Bwanji uti, Sindinaipitsidwa,
sindinatsata Abaala? Ona njira yako m'cigwa, dziwa cimene
wacicita; ndiwe ngamila yothamanga yoyenda m'njira
zace; 24mbidzi yozolowera m'cipululu, yopumira mphepo pakufuna
pace; pokomana nayo ndani adzaibweza? onse amene aifuna
sadzadzilemetsa; adzaipeza m'mwezi wace. 25Kaniza phazi lako
lisakhale losabvala nsapato, ndi m'mero mwako musakhale ndi
ludzu; koma unati, Palibe ciyembekezo, iai; pakuti ndakonda
alendo, ndipo ndidzatsata pambuyo pao. 26Monga mbala iri ndi
manyazi pamene igwidwa, comweco nyumba ya Israyeli iri ndi
manyazi; iwo, mafumu ao, akuru ao, ansembe ao, ndi aneneri
ao; 27amene ati kwa mtengo, Iwe ndiwe atate wanga; ndi kwa
mwala, Wandibala; pakuti anandipatsa Ine mbuyo, si nkhope yao;
koma m'nthawi ya kubvutidwa kwao adzati, Ukani,
tipulumutseni. 28Koma iri kuti milungu yako imene wadzipangira?
Iuke, ikupulumutse iwe m'nthawi ya kubvutidwa kwako; pakuti
milungu yako ilingana ndi kucuruka kwa midzi yako, Yuda iwe.
29Cifukwa canji mudzatsutsana ndi Ine nonse? mwandilakwira Ine,
ati Yehova. 30Ndapanda ana anu mwacabe; sanamvera kulanga;
lupanga lanu ladya aneneri anu, monga mkango
wakuononga. 31Mbadwo inu, taonani mau a Yehova. Kodi ndakhala
kwa Israyeli cipululu? Kapena dziko la mdima woti bii? Cifukwa ninji
ati anthu anga, Tamasuka sitidzabweranso konse kwa Inu? 32Kodi
angathe namwali kuiwala zokometsera zace, kapena mkwatibwi
zobvala zace? koma anthu anga andiiwala Ine masiku
osawerengeka. 33Kodi sukonzadi njira yako kufunafuna cilakolako?
cifukwa cace waphunzitsa akazi oipa njira zako. 34Ndiponso
m'nsaru zako wapezeka mwazi wa miyoyo ya aumphawi
osacimwa; sunawapeza pakuboola, koma ponsepo. 35Koma unati,
Ndiri wosacimwa ndithu; mkwiyo wace wacoka pa ine. Taona,
ndidzakuweruza iwe, cifukwa uti, Sindinacimwa. 36Bwanji
uyendayenda kwambiri ndi kusintha njira yako? udzacitanso
manyazi ndi Aigupto monga unacita manyazi ndi Asuri. 37Koma
udzaturuka kwa iyenso, manja ako pamtu pako; pakuti Yehova
wakana zokhulupirira zako, ndipo sudzapindula m'menemo.

©The Bible Society of Malawi, 1992

1Amati, Ngati mwamuna acotsa mkazi wace, ndipo amcokera iye,
nakhala mkazi wa wina, kodi adzabweranso kwa mkaziyo? dzikolo
kodi silidzaipitsidwa? Koma iwe wacita dama ndi mabwenzi ambiri;
koma bweranso kwa Ine, ati Yehova. 2Kwezera maso ako ku mapiri
oti se, nuone: sanagona ndi iwe kuti? Panjira wakhalira iwo, monga
M-arabu m'cipululu; ndipo waipitsa dziko ndi zigololo zako, ndi zoipa
zako. 3Ndipo mvula yakanidwa, ndipo panalibe mvula ya masika;
ndipo unali ndi nkhope ya mkazi wadama, unakana manyazi. 4Kodi
kuyambira tsopano sudzapfuulira kwa Ine, Atate wanga,
wotsogolera ubwana wanga ndinu? 5Kodi adzasunga mkwiyo wace
ku nthawi zonse? Kodi adzakudikira mpaka cimariziro? Taona,
wanena ndi kucita zoipa monga unatero.

Abwere kwa Yehova anthu olowererawo

6Ndipo Yehova anati kwa ine masiku a Yosiya mfumu, Kodi waona
cimene wacicita Israyeli, wobwerera m'mbuyo? Wakwera pa mapiri
atari onse, ndi patsinde pa mitengo yaiwisi yonse, ndi kucita dama
pamenepo. 7Ndipo ndinati atacita zimenezo zonse, Adzabwera kwa
Ine; koma sanabwere, ndipo mphwace wonyenga, Yuda,
anaona. 8Ndipo ndinaona, kuti, ndingakhale ndikamcotsa Israyeli
wobwerera m'mbuyo, ndi kumpatsa kalata wacilekaniro cifukwa ca
kucita cigololo iye, mphwace Yuda wonyenga sanaope, koma iye
yemwe ananka nacita dama. 9Ndipo kunali kuti mbiri ya dama lace
inaipitsa dziko, ndipo anacita cigololo ndi miyala ndi
mitengo. 10Ndipo zingakhale zonsezi mphwace wonyenga
sanabwera kwa Ine ndi mtima wace wonse, koma monama, ati
Yehova. 11Ndipo Yehova anati kwa ine, Israyeli wobwerera
anadzionetsa wolungama kopambana ndi Yuda wonyenga, 12Pita;
nulalikire mau awa kuyang'ana kumpoto, ndi kuti, Bwera iwe
Israyeli wobwerera, ati Yehova; sindidzakuyang'anira iwe ndi
kukwiya; pakuti Ine ndiri wacifundo, ati Yehova, sindidzakhala nako
kukwiya ku nthawi zonse. 13Koma bvomereza zoipa zako, kuti
walakwira Yehova Mulungu wako, ndi kupatukira mwa alendo
patsinde pa mitengo yaiwisi yonse, ndipo sunamvera mau anga,
ati Yehova. 14Bwerani, ananu obwerera, ati Yehova; pakuti Ine
ndine mbuye wanu; ndipo ndidzakutengani inu mmodzi mmodzi
wa pa mudzi uli wonse, ndi awiri awiri a pa banja liri lonse, ndi
kukutengerani ku Ziyoni; 15ndipo ndidzakupatsani inu abusa
monga mwa mtima wanga, adzakudyetsani inu nzeru ndi
luntha. 16Ndipo padzaoneka, pamene mudzakhala ambiri ndi
kucuruka m'dzikomo masiku awo, ati Yehova, sadzatinso konse,
Likasa la cipangano ca Yehova; silidzalowa m'mtima;
sadzalikumbukira; sadzanka kukaliona, sadzacitanso konse. 17Pa
nthawi yomweyo adzacha Yerusalemu mpando wa Yehova; ndipo

mitundu yonse idzasonkhanidwa kumeneko, ku dzina la Yehova, ku Yerusalemu; ndipo sadzayendanso konse m'kuumirira kwa mtima wao woipa. 18Masiku omwewo nyumba ya Yuda idzayenderana ndi nyumba ya Israyeli, ndipo adzaturuka pamodzi ku dziko la kumpoto kunka ku dziko limene ndinapatsa makolo anu kuti alowemo. 19Koma Ine ndinati, Ndidzakuika iwe bwanji mwa ana, ndi kupatsa iwe dziko lokondweretsa, colowa cabwino ca makamu a mitundu ya anthu? ndipo ndinati mudzandicha Ine, Atate wanga; osatembenuka kuleka kunditsata Ine. 20Ndithu monga mkazi acokera mwamuna wace monyenga, comweco mwacita ndi Ine monyenga, inu nyumba ya Israyeli, ati Yehova. 21Mau amveka pa mapiri oti se, kulira ndi kupempha kwa ana a Israyeli; pakuti anaipitsa njira yao, naiwala Yehova Mulungu wao. 22Bwerani, ana inu obwerera, ndidzaciritsa mabwerero anu. Taonani, tadza kwa Inu; pakuti ndinu Yehova Mulungu wathu. 23Ndithu akhulupirira mwacabe cithandizo ca kuzitunda, ndi phokoso la kumapiri; ndithu mwa Yehova Mulungu wathu muli cipulumutso ca Israyeli, 24Ndipo cocititsa manyazi cinathetsa nchito za atate athu kuyambira ubwana wathu; nkhosa zao ndi zoweta zao, ana ao amuna ndi akazi. 25Tigone m'manyazi athu, kunyala kwathu kutipfunde ife; pakuti tamcimwira Yehova Mulungu wathu, ife ndi makolo athu, kuyambira ubwana wathu kufikira lero lomwe; ndipo sitidamvera mau a Yehova Mulunguwathu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

1Ngati udzabwera, Israyeli, ati Yehova, udzabwera kwa Ine; ndipo
ngati udzacotsa zonyansa zako pamaso panga
sudzacotsedwa. 2Ndipo udzalumbira, Pali Yehova m'zoonadi,
m'ciweruziro, ndi m'cilungamo; ndipo mitundu ya anthu
idzadzidalitsa mwa Iye, ndipo mwa Iye adzatamandira.

Adani acilendo adzagwera dziko la Yuda

3Pakuti Yehova atero kwa anthu a Yuda ndi kwa Yerusalemu, Limani
masala anu, musabzale paminga. 4Mudzidulire nokha kwa Yehova,
cotsani khungu la mitima yanu, amuna inu a Yuda ndi okhala
m'Yerusalemu; ukali wanga ungaturuke ngati moto, ungatenthe
kuti sangathe kuuzima, cifukwa ca kuipa kwa macitidwe
anu. 5Nenani m'Yuda, lalikirani m'Yerusalemu, ndi kuti, Ombani
lipenga m'dzikomo; pfuulani, ndi kuti, Sonkhanani pamodzi, tilowe
m'midzi ya malinga. 6Kwezani mbendera kuyang'ana ku Ziyoni;
thawani kuti mupulumuke, musakhale; pakuti ndidza ndi coipa
cocokera kumpoto ndi kuononga kwakukuru. 7Mkango wakwera
kuturuka m'nkhalango mwace, ndipo woononga amitundu ali
panjira, waturuka m'mbuto mwace kuti acititse dziko lako bwinja,
kuti midzi yako ipasuke mulibenso wokhalamo. 8Pamenepo, bvalani
ciguduli, lirani ndi kubuula; pakuti mkwiyo wakuopsya wa Yehova
sunabwerera pa ife. 9Ndipo padzakhala tsiku lomwelo, ati Yehova,
kuti mtima wa mfumu udzatayika, ndi mitima ya akuru; ndipo
ansembe adzazizwa, ndi aneneri adzadabwa. 10Ndipo ndinati, Ha,
Yehova Mulungu! ndithu mwanyenga kwambiri anthu awa ndi
Yerusalemu, ndi kuti, Mu'dzalandira mtendere; koma lupanga
lafikira pamoyo. 11Pa nthawi yomweyo adzati kwa anthu awa ndi
kwa Yerusalemu, Mphepo yotentha yocokera ku mapiri oti se
m'cipululu yopita kwa mwana wamkazi wa anthu anga,
yosaungula, yosayeretsa; 12mphepo yolimba yocokera kumeneko
idzandifika ine; tsopanonso ndidzaweruza iwo
maweruzo. 13Taonani, adzadza ngati mitambo, ndi magareta ace
ngati kabvumvulu; akavalo ace athamanga kopambana mphungu,
Tsoka ife! pakuti tapasuka. 14Iwe Yerusalemu, utsuke mtima wako
kucotsa zoipa kuti upulumuke. Maganizo ako acabe agona mwako
masiku angati? 15Pakuti mau anena m'Dani nalalikira nsautso
m'phiri la Efraimu: 16Mukumbutse mitundu ya anthu; taonani,
lalikirani Yerusalemu, kuti owazinga ndi nkhondo afumira ku dziko
lakutari, nainenera midzi ya Yuda mau ao. 17Monga adindo a
m'munda amzinga iye; cifukwa andipandukira Ine, ati
Yehova. 18Njira yako ndi nchito zako zinakucitira izi; ici ndico coipa
cako ndithu; ciri cowawa ndithu, cifikira ku mtima wako.
19Matumbo anga, matumbo anga! ndipoteka pamtima panga peni
peni; mtima wanga sukhala pansi m'kati mwanga; sindithai

kutonthola; pakuti wamva, moyo wanga, mau a lipenga, mbiri ya nkhondo. 20Alalikira cipasuko cilalikire; pakuti dziko lonse lafunkhidwa; mahema anga afunkhidwa dzidzidzi, ndi nsaru zanga zocinga m'kamphindi. 21Kufikira liti ndidzaona mbendera, ndi kumva kulira kwa lipenga? 22Pakuti anthu anga apusa, sandidziwa Ine; ali ana opulukira sazindikira; ali ocenjera kucita coipa koma kucita cabwino sakudziwa.
23Ndinaona dziko lapansi, ndi rpo taona, linali lopasuka lopanda kanthu; ndipo ndinaona kumwamba, kunalibe kuunika. 24Ndinaona mapiri, taona ananthunthumira; ndipo zitunda zonse zinagwedezeka. 25Ndinaona, ndipo taona, panalibe munthu, ndi mbalame zonse zakumwamba zinathawa. 26Ndinaona, ndipo taona, munda wazipatso unali cipululu, ndipo midzi yace yonse inapasuka pamaso pa Yehova, ndi pamaso pa mkwiyo wace woopsya. 27Pakuti Yehova atero, Dziko lonse lidzakhala bwinja koma sindidzatsirizitsa. 28Cifukwa cimeneco dziko lidzalira maliro, ndipo kumwamba kudzada; cifukwa ndanena, ndatsimikiza mtima, sindinatembenuka, sindidzabwerera pamenepo. 29Mudzi wonse uthawa m'phokoso la apakavalo ndi amauta; adzalowa m'nkhalango, adzakwera pamiyala; midzi yonse idzasiyidwa, ndipo simudzakhala munthu m'menemo. 30Nanga iwe, udzacita ciani pamene udzafunkhidwa? Ngakhale udzibveka ndi zofiira, ngakhale udzibveka ndi zokometsera zagolidi, ngakhale udzikuzira maso ako ndi kupaka, udzikometsera pacabe; mabwenzi adzakunyoza adzafuna moyo wako. 31Pakuti ndamva kubuula ngati kwa mkazi wobala, ndi msauko ngati wa mkazi wobala mwana wace woyamba, mau a mwana wamkazi wa Ziyoni wakupuma mosiyiza, wakutambasula manja ace, ndi kuti, Tsoka ine tsopano! pakuti moyo wanga walefuka cifukwa ca ambanda.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Malango a Mulungu pa Ayuda cifukwa ca zoipa zao zonse

1Thamangani inu kwina ndi kwina m'miseu ya Yerusalemu,
taonanitu, dziwani, ndi kufunafuna m'mabwalo ace, kapena
mukapeza munthu, kapena alipo wakucita zolungama, wakufuna
coonadi; ndipo ndidzamkhululukira. 2Ndipo ngakhale ati, Pali
Yehova; komatu alumbira monama. 3Yehova Inu, maso anu sali
pacoonadi kodi? munawapanda iwo, koma sanaphwetekedwa
mtima; munawatha iwo, koma akana kudzudzulidwa; alimbitsa
nkhope zao koposa mwala; akana kubwera. 4Ndipo ine ndinati,
Ndithu amenewo ali aumphawi; ali opusa; pakuti sadziwa njira ya
Yehova, kapena ciweruzo ca Mulungu wao. 5Ine ndidzanka kwa
akuru, ndidzanena ndi iwo; pakuti adziwa njira ya Yehova, ndi
ciweruzo ca Mulungu wao. Koma awa anabvomerezana natyola
gori, nadula zomangira zao. 6Cifukwa cace mkango woturuka
m'nkhalango udzawapha, ndi mmbulu wa madzulo udzawafunkha,
nyalugwe adzakhalira m'midzi mwao, onse amene aturukamo
adzamwetulidwa; pakuti zolakwa ziri zambiri, ndi mabwerero ao
acuruka. 7Bwanji ndidzakhululukira iwe? pamenepo ana ako
andisiya Ine, nalumbira pa iyo yosati milungu; pamene
ndinakhutitsa iwo, anacita cigololo, nasonkhana masonkhano
m'nyumba za adama. 8Anali onga akavalo okhuta mamawa; yense
wakumemesera mkazi wa mnansi wace. 9Kodi sindidzawalanga
cifukwa ca zimenezi? ati Yehova; kodi moyo wanga sudzabwezera
cilango mtundu woterewu?
10Kwerani pa makoma ace nimupasule; koma musatsirize konse;
cotsani nthambi zace pakuti siziri za Yehova. 11Pakuti nyumba ya
Israyeli ndi nyumba ya Yuda zinandicitira monyenga kwambiri, ati
Yehova. 12Akana Yehova, ndi kuti, Si ndiye; coipa sicidzatifika ife;
sitidzaona kapena lupanga kapena njala; 13ndipo aneneri
adzasanduka mphepo, ndipo mwa iwo mulibe mau; comweco
cidzacitidwa ndi iwo. 14Cifukwa cace Yehova Mulungu wa makamu
atero, Cifukwa munena mau awa, taona, ndidzayesa mau anga
akhale m'kamwa mwako ngati moto, anthu awa ndidzayesa
nkhuni, ndipo udzawatha iwo. 15Taonani, ndidzatengera pa inu
mtundu wa anthu akutari, inu nyumba ya Israyeli, ati Yehova; ndi
mtundu wolimba, ndi mtundu wakalekale, mtundu umene cinenero
cace simudziwa, ngakhale kumva zonena zao. 16Phodo lao liri ngati
manda apululu, onsewo ndiwo olimba. 17Adzadya zokolola zako,
ndi mkate wako, umene ana ako amuna ndi akazi ayenera kudya;
adzadya nkhosa zako ndi zoweta zako; adzadya mphesa zako ndi
nkhuyu zako; adzapasula ndi lupanga midzi yamalinga yako, imene
ukhulupiriramo. 18Koma masiku onsewo, ati Yehova,
sindidzatsirizitsa konse ndi iwe. 19Ndipo padzakhala: pamene

mudzati, Cifukwa canji Yehova Mulungu wathu aticitira ife zonse izi? ndipo udzayankha kwa iwo, Monga ngati mwandisiya Ine, ndi kutumikira milungu yacilendo m'dziko lanu, momwemo mudzatumikira alendo m'dziko siliri lanu.
20Nenani ici m'nyumba ya Yakobo, lalikirani m'Yuda,
kuti, 21Tamvanitu ici, inu anthu opusa, ndi opanda nzeru; ali ndi maso koma osaona, ali ndi makutu koma osamva; 22Kodi simundiopa Ine? ati Yehova: simudzanthunthumira pamaso pa Ine, amene ndinaika mcenga cilekaniro ca nyanja, ndi lemba lamuyaya kuti isapitirirepo? ndipo ngakhale mafunde ace acita gabvigabvi, alephera; ngakhale akokoma, sangathe kupitirirapo. 23Koma anthu awa ali ndi mtima woukirana ndi wopikisana; anapanduka nacoka. 24Ndipo sanena m'mtima mwao, Tiopetu Yehova Mulungu wathu wopatsa mvula yoyamba ndi yamasika, m'nyengo yace; atisungira ife masabata olamulidwa a masika. 25Mphulupulu zanu zacotsa zimenezi, ndi zocimwa zanu zakukanitsani inu zinthu zabwino. 26Pakuti mwa anthu anga aoneka anthu oipa; adikira monga akucha misampha; acha khwekhwe, agwira anthu. 27Monga cikwere codzala ndi mbalame, comweco nyumba zao zadzala ndi cinyengo; cifukwa cace akula, alemera, 28Anenepa, anyezimira; inde apitiriza kucita zoipa; sanenera ana amasiye mlandu wao, kuti apindule; mlandu wa aumphawi saweruza. 29Sindidzawalanga kodi cifukwa ca zimenezi? ati Yehova; kodi moyo wanga sudzabwezera cilango mtundu wotere?
30Codabwitsa ndi coopsya caoneka m'dzikomo; 31aneneri anenera monyenga nathandiza ansembe pakulamulira kwao; ndipo anthu anga akonda zotere; ndipo mudzacita ciani pomarizira pace?

©The Bible Society of Malawi, 1992

Acenjezedwa kuti adani adzamangira Yerusalemu misasa

1Ananu a Benjamini, pulumukani pothawa pakati pa Yerusalemu,
ombani lipenga m'Tekoa, kwezani cizindikiro m'Beti-hakeremu;
pakuti caoneka coipa coturuka m'mpoto ndi kuononga
kwakukulu. 2Ndidzacotsa mwana wamkazi wa Ziyoni mkazi
wokoma ndi wololopoka. 3Abusa ndi nkhosa zao adzadza kwa iye;
adzamanga mahema ao pomzinga iye; adzadya yense pokhala
pace. 4Lalikirani nkhondo yakumenyana ndi iye; ukani, tikwere
pakati pa usana. Tsoka kwa ife! pakuti dzuwa lapendeka, mithunzi
ya madzulo yatambasuka. 5Ukani, tiyende usiku, tipasule nyumba
zace. 6Pakuti Yehova wa makamu atero, Dulani mitengo, unjikani
nthumbira pomenyana ndi Yerusalemu; mudzi wakudzalangidwa
ndi uwu; m'kati mwace modzala nsautso. 7Monga kasupe aturutsa
madzi ace, camweco aturutsa zoipa zace; ciwawa ndi kufunkha
zimveka m'kati mwace; pamaso panga masiku onse pali kulira ndi
mabala. 8Ulangizidwe, Yerusalemu, ungakucokere moyo wanga,
ndingakuyese iwe bwinja, dziko losakhalamo anthu.
9Yehova wa makamu atero, Adzakunkha otsalira a Israyeli monga
mpesa; bweza dzanja lako monga wakuchera mphesa m'mitanga
yace. 10Ndidzanena ndi yani, ndidzacita mboni kwa yani, kuti
amve? Taona khutu lao liri losadulidwa, ndipo sangathe kumva;
taona, mau a Yehova awatonzetsa iwo; sakondwera nao. 11Cifukwa
cace ndadzala ndi ukali wa Yehova; ndalema ndi kudzikaniza;
tsanulirani pa ana a pabwalo, ndi pa masonkhano a anyamata,
pakuti ngakhale mwamuna ndi mkazi wace adzatengedwa,
okalamba ndi iye amene acuruka masiku ace. 12Nyumba zao
zidzasanduka za ena, pamodzi ndi minda yao ndi akazi ao; pakuti
ndidzatambasula dzanja langa pa okhala m'dziko, ati
Yehova. 13Pakuti kuyambira wamng'ono kufikira wamkuru onse
akhala akusirira; ndiponso kuyambira mneneri kufikira wansembe
onse acita monyenga, 14Ndiponso apoletsa bala la anthu anga
pang'onong'ono, ndi kuti, Mtendere, mtendere; koma palibe
mtendere. 15Kodi anakhala ndi manyazi pamene anacita
conyansa? lai, sanakhala konse ndi manyazi, sanathe kunyala;
cifukwa cace adzagwa mwa iwo akugwa; panthawi pamene
ndidzafika cwa iwo, aclzagwetsedwa, ati Yehova.
16Yehova atero, Imani m'njira ndi kuona, funsani za mayendedwe
akale, m'menemo muli njira yabwino, muyende m'menemo, ndipo
mudzapeza mpumulo wa miyoyo yanu; koma anati,
Sitidzayendamo. 17Ndipo ndinaika alonda oyang'anira inu, ndi kuti,
Mverani mau a lipenga; koma anati, Sitidzamvera. 18Cifukwa cace
tamverani, amitundu inu, dziwani, msonkhano inu, cimene ciri
mwa iwo. 19Tamva, dziko lapansi iwe; taona, Ine ndidzatengera

coipa pa anthu awa, cipatso ca maganizo ao, pakuti sanamvera mau anga, kapena cilamulo canga, koma wacikana. 20Cofukiza cindifumiranji ku Seba, ndi nzimbe ku dziko lakutari? nsembe zopsereza zanu sizindisekeretsa, nsembe zophera zanu sizindikondweretsa Ine. 21Cifukwa cace atero Yehova, Taona, ndidzaikira anthuwa zopunthwitsa; ndipo atate ndi ana adzakhumudwa nazo pamodzi; munthu ndi mnzace adzatayika. 22Yehova atero, Taona, mtundu wa anthu ucokera kumpoto; ndi mtundu waukuru adzaukitsidwa ku malekezero a dziko lapansi. 23Agwira uta ndi nthungo; ali ankharwe, alibe cifundo; mau ao aphokosera ngati nyanja, akwera pa akavalo; aguba monga anthu ofuna kumenyana nkhondo ndi iwe, mwana wamkazi wa Ziyoni. 24Tamva ife mbiri yace; manja athu alefuka, yatigwira nkhawa ndi zowawa ngati za mkazi wobala. 25Usaturukire kumunda, usayenda m'njira; pakuti lupanga la amaliwongo ndi mantha ali m'mbali zonse. 26Iwe mwana wamkazi wa anthu anga, udzibveke ndi ciguduli, ndi kubvimbvinika m'phulusa; ulire maliro ngati a mwana wamwamuna wa yekha, kulira kowawa koposa; pakuti wakufunkha adzatifikira ife motidzidzimutsa. 27Ndakuyesa iwe nsanja ndi linga mwa anthu anga, kuti udziwe ndi kuyesa njira yao. 28Onse ali opikisana ndithu, ayendayenda ndi maugogodi; ndiwo mkuwa ndi citsulo; onsewa acita mobvunda; 29mbvukuto yatenthedwa ndi moto; mthobvu watha ndi moto wa ng'anjo; ayenga cabe; pakuti oipa sacotsedwa. 30Anthu adzawacha nthale ya siliva, pakuti Yehova wakana iwo.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Mneneri alikuima pa cipata ca Kacisi, achula mau akulonieza ndi akuopsa

1Mau amene anadza kwa Yeremiya kucokera kwa Yehova,
kuti, 2Ima m'cipata ca nyumba ya Yehova, lalikira m'menemo mau
awa, ndi kuti, Tamvani mau a Yehova, inu nonse a Yuda, amene
alowa m'zipata izi kuti mugwadire Yehova. 3Yehova wa makamu
atero, Mulungu wa Israyeli, Konzani njira zanu ndi macitidwe anu,
ndipo ndidzakukhalitsani inu m'malo ano. 4Musakhulupirire mau
onama, kuti, Kacisi wa Yehova, kacisi wa Yehova, kacisi wa Yehova
ndi awa. 5Pakuti mukakonzatu njira zanu ndi macitidwe anu; ndi
kuweruzatu milandu ya munthu ndi mnansi wace; 6ndi kuleka
kutsendereza mlendo, ndi wamasiye, ndi mkazi wamasiye,
osakhetsa mwazi wosacimwa m'malo muno, osatsata milungu yina
ndi kudziipitsa nayo; 7ndipo ndidzakukhazikani inu m'malo muno,
m'dziko limene ndinapatsa makolo anu, kuyambira kale lomwe
kufikira muyaya, 8Taonani, mukhulupirira mau onama,
osapindulitsa. 9Kodi mudzapha, ndi kuba, ndi kucita cigololo, ndi
kulumbira zonama, ndi kupereka nsembe kwa Baala, ndi kutsata
milungu yina imene simunaidziwa, 10ndi kudza ndi kuima pamaso
panga m'nyumba yino, imene ichedwa dzina langa, ndi kuti,
Talanditsidwa; kuti mucite zonyansa izi? 11Kodi nyumba yino,
imene ichedwa dzina langa, ikhala phanga la okwatula pamaso
panu? Taona, Ine ndaciona, ati Yehova. 12Koma pitani tsopano ku
malo anga amene anali m'Silo, m'mene ndinaikamo dzina langa
poyamba paja, ndi kuona cimene ndinacitira cifukwa ca zoipa za
anthu anga Israyeli. 13Ndipo tsopano, cifukwa munacita nchito
zonsezi, ati Yehova, ndipo ndinanena kwa inu, ndi kuuka mamawa
ndi kunena, koma simunamva; ndipo ndinakuitanani inu, koma
simunayankha; 14cifukwa cace ndidzaicitira nyumba iyi, imene
ichedwa dzina langa, imene mukhulupirirayi, ndipo ndidzacitira
malo amene ndinakupatsani inu ndi makolo anu, monga ndinacitira
Silo. 15Ndipo ndidzakucotsani inu pamaso panga, monga
ndinacotsa abale anu onse, mbeu zonse za Efraimu.
16Cifukwa cace iwe usapempherere anthu awa, usawakwezere iwo
mpfuu kapena pemphero, usandipembedze; pakuti Ine
sindidzakumvera iwe. 17Kodi suona iwe cimene acicita m'midzi ya
Yuda ndi m'miseu ya Yerusalemu? 18Ana atola nkhuni, atate
akoleza moto, akazi akanyanga ufa, kuti aumbe mikate ya mfumu
yaikazi ya kumwamba, athirire milungu yina nsembe yothira, kuti
autse mkwiyo wanga. 19Kodi autsa mkwiyo wanga? ati Yehova;
kodi sadziutsira okha manyazi a nkhope zao? 20Cifukwa cace, ati
Ambuye Mulungu, Taonani, mkwiyo wanga ndi ukali wanga

udzathiridwa pa malo ano, pa anthu, ndi pa nyama, ndi pa mitengo
ya m'munda, ndi pa zipatso zapansi; ndipo udzatentha osazima.
21Atero Yehova wa makamu, Mulungu wa Israyeli; Ikani zopereka
zopsereza zanu pa nsembe zophera zanu, nimudye
nyama. 22Pakuti sindinanena kwa makolo anu, tsiku lija
ndinawaturutsa m'dziko la Aigupto, ngakhale kuwauza nsembe
zopsereza kapena zophera; 23koma cinthu ici ndinawauza, kuti,
Mverani mau anga, ndipo ndidzakhala Mulungu wanu, ndipo inu
mudzakhala anthu anga; nimuyende m'njira yonse imene
ndakuuzani inu, kuti cikukomereni. 24Koma sanamvera, sanachera
khutu, koma anayenda m'upo ndi m'kuuma kwa mtima wao woipa,
nabwerera cambuyo osayenda m'tsogolo. 25Ciyambire tsiku limene
makolo anu anaturuka m'dziko la Aigupto kufikira lero lino,
ndatumiza kwa inu atumiki anga onse, aneneri, tsiku ndi tsiku,
kuuka mamawa ndi kuwatumiza iwo; 26koma sanandimvera Ine,
sanacherakhutu lao, koma anaumitsa khosi lao; anaipa koposa
makolo ao.
27Ndipo uzinena kwa iwo mau awa onse, koma sadzakumvera iwe;
ndipo udzawaitananso; koma sadzakuyankha iwe. 28Ndipo udzati
kwa iwo, Umene ndi mtundu wosamvera mau a Yehova Mulungu
wao, wosalola kulangizidwa, coonadi catha, cadulidwa pakamwa
pao.

Zoopsa za Tofeti

29Senga tsitsi lako, iwe Yerusalemu, nulitaye, nukweze maliro pa
mapiri oti se; pakuti Yehova wakana ndi kusiya mbadwo umene
aukwiyira. 30Pakuti ana a Yuda anacita coipa pamaso panga, ati
Yehova; naika zonyansa zao m'nyumba yochedwa dzina langa, kuti
alipitse. 31Namanga akacisi a ku Tofeti, kuli m'cigwa ca mwana wa
Hinomu, kuti atenthe m'moto ana ao amuna ndi akazi; cimene
sindinauza iwo, sicinalowa m'mtima mwanga. 32Cifukwa cace,
taonani, masiku alikudza, ati Yehova, ndipo sadzachedwanso Tofeti,
kapena Cigwa ca mwana wa Hinomu, koma Cigwa ca Kuphera;
pakuti adzataya m'Tofeti, kufikira malo akuikamo
adzasowa. 33Ndipo mitembo ya anthu awa idzakhala zakudya za
mbalame za mlengalenga, ndi za zirombo za dziko lapansi; palibe
amene adzaziopsa. 34Ndipo ndidzaletsa m'midzi ya Yuda, ndi
m'miseu ya Yerusalemu, mau akukondwa ndi mau akusekera, ndi
mau a mkwati ndi mau a mkwatibwi; pakuti dziko lidzasanduka
bwinja.

©The Bible Society of Malawi, 1992

1Nthawi yomweyo, ati Yehova, adzaturutsa m'manda mwao mafupa
a mafumu a Yuda, ndi mafupa a akuru ace, ndi mafupa a ansembe,
ndi mafupa a aneneri, ndi mafupa a okhala m'Yerusalemu, 2ndipo
udzawayanika padzuwa, ndi pamwezi, ndi pa khamu lonse la
kuthambo, limene analikonda, ndi kulitumikira, ndi kulitsata, ndi
kulifuna, ndi kuligwadira; sadzasonkhanidwa, sadzaikidwa;
adzakhala ndowe panthaka. 3Ndipo otsala onse amene akutsala pa
banja loipa ili adzasankha imfa koposa moyo, ndiwo amene atsala
m'malo monse m'mene ndinawaingiramo, ati Yehova wa makamu.
Kulowerera kwa anthu a Mulungu, kulangidwa kudzafikadi
4Ndiponso udzati kwa iwo, Atero Yehova, Kodi adzagwa,
osaukanso? Kodi wina adzacoka, osabweranso? 5Bwanji abwerera
anthu awa a Yerusalemu cibwererere? agwiritsa cinyengo, akana
kubwera. 6Ndinachera khutu, ndinamva koma sananena bwino;
panalibe munthu amene anatembenuka kusiya zoipa zace, ndi
kuti, Ndacita ciani? yense anatembenukira njira yace, monga
akavalo athamangira m'nkhondo. 7Inde, cumba ca mlengalenga
cidziwa nyengo zace; ndipo njiwa ndi namzeze ndi cingaru
ziyang'anira nyengo yakufika kwao; koma anthu anga sadziwa
ciweruziro ca Yehova. 8Bwanji muti, Tiri ndi nzeru ife, ndi malamulo
a Yehova ali ndi ife? Koma, taona, peni lonyenga la alembi lacita
zonyenga, 9Anzeru ali ndi manyazi, athedwa nzeru nagwidwa;
taonani, akana mau a Yehova; ali nayo nzeru yotani? 10Cifukwa
cace ndidzapereka akazi ao kwa ena, ndi minda yao kwa iwo
adzalowamo; pakuti onse kuyambira wamng'ono kufikira wamkuru
asirirasirira; kuyambira mneneri kufikira wansembe onse acita
zonyenga. 11Ndipo analipoletsa pang'ono bala la mwana wamkazi
wa anthu anga, ndi kuti, Mtendere, mtendere; posakhala
mtendere. 12Kodi anakhala ndi manyazi pamene anacita
zonyansa? iai, sanakhala ndi manyazi, sananyala; cifukwa cace
adzagwa mwa iwo amene akugwa, nthawi ya kuyang'aniridwa
kwao adzagwetsedwa, ati Yehova. 13Kuwatha ndidzawathetsa iwo,
ati Yehova, sipadzakhala mphesa pampesa, kapena nkhuyu
pamkuyu, ndipo tsamba lidzafota, ndipo zinthu ndinawapatsa
zidzawacokera. 14Tikhaliranji ife? tasonkhanani, tilowe m'midzi
yamalinga, tikhale cete m'menemo; pakuti Yehova Mulungu wathu
watikhalitsa ife cete, natipatsa ife madzi a ndulu timwe, pakuti
tamcimwira Yehova. 15Tinayang'anira mtendere, koma panalibe
zabwino; ndi nthawi ya moyo, ndipo taona kuopsedwa! 16Kumina
kwa akavalo ace kunamveka ku Dani; dziko lonse linanthunthumira
pa kulira kwa akavalo acewo olimba; cifukwa afika, nadya dziko ndi
zonse za momwemo; mudzi ndi amene akhalamo. 17Pakuti,

taonani, ndidzatumiza pa inu njoka, mphiri, zosalola kuitanidwa;
ndipo zidzakulumani inu, ati Yehova.
18Ha, ndikadatonthoza mtima wanga kuletsa cisoni cace! mtima
wanga walefuka m'kati mwa ine. 19Taonani, mau a kulira kwa
mwana wamkazi wa anthu anga ocokera ku dziko lakutari: Kodi
m'Ziyoni mulibe Yehova? Kodi mulibe Mfumu yace? Cifukwa canji
andiputa Ine ndi mafano ao osema, ndi zacabe zacilendo? 20Masika
apita, mphakasa yatha, ndipo ife sitinapulumutsidwe. 21Bala la
mwana wamkazi wa anthu anga ndaphwetekwa nalo; ndada
mtima; kudabwa kwandigwira. 22Kodi mulibe bvunguti m'Gileadi?
Kodi mulibe sing'anga m'menemo; analekeranji kucira mwana
wamkazi wa anthu anga?

©The Bible Society of Malawi, 1992

1Ha, mutu wanga ukadakhala madzi, ndi maso anga kasupe wa
misozi, kuti usana ndi usiku ndilirire ophedwa a mwana wamkazi wa
anthu anga! 2Ha, ndikadakhala ndi cigono ca anthu aulendo
m'cipululu; kuti ndisiye anthu anga, ndiwacokere, pakuti onse ali
acigololo msonkhano wa anthu aciwembu. 3Ndipo apinda lilime lao
ngati uta wao, liname; koma akula mphamvu m'dzikomo, koma si
pacoonadi; pakuti alinkunkabe nacita zoipa, ndipo sandidziwa Ine,
ati Yehova. 4Mucenjere naye yense mnansi wace, musakhulupirire
yense mbale wace; pakuti abale onse amanyenga, ndipo anansi
onse adzayenda ndi maugogodi. 5Ndipo yense adzanyenga mnansi
wace, osanena coonadi; aphunzitsa lilime lao kunena zonama;
nadzithodwetsa kucita zoipa. 6Ukhala pakati pa manyengo
m'manyengo; akana kundidziwa, ati Yehova.

Acenjezedwa za kuonongeka ndi kutengedwa ukapolo

7Cifukwa cace atero Yehova wa makamu, Taonani,
ndidzawasungunula, ndi kuwayesa, pakuti ndidzacitanji, cifukwa ca
mwana wamkazi wa anthu anga? 8Lilime lao ndi mubvi wakuphera;
linena manyengo; wina anena mtendere ndi mnansi wace
pakamwa pace, koma m'mtima mwace amlalira. 9Kodi
sindidzawalanga cifukwa ca izi? ati Yehova; kodi moyo wanga
sudzabwezera cilango mtundu wotere?
10Cifukwa ca mapiri ndidzagwa misozi ndi kulira, cifukwa ca
mabusa a cipululu ndidzacita maliro, cifukwa apserera, kuti anthu
sangathe kupitirirapo; ndiponso anthu sangathe kumva mau a
ng'ombe zao; mbalame za mlengalenga ndi nyama zathawa,
zapita. 11Ndipo ndidzayesa Yerusalemu miyulu, mbuto ya
ankhandwe; ndipo ndidzayesa midzi ya Yuda bwinja, lopanda
wokhalamo. 12Wanzeru ndani, kuti adziwe ici? ndani iye amene
kamwa la Yehova lanena naye, kuti acilalikire? cifukwa cace dziko
litha ndi kupserera monga cipululu, kuti anthu asapitemo?
13Ndipo Yehova ati, Cifukwa asiya cilamulo canga ndinaciika
pamaso pao, ndipo sanamvera mau anga, osayenda
m'menemo; 14koma anatsata kuuma kwa mtima wao, ndi Baala,
monga makolo ao anawaphunzitsa; 15cifukwa cace atero Yehova
wa makamu, Mulungu wa Israyeli, Taonani, ndidzadyetsa anthu
awa civumulo, ndi kuwamwetsa madzi
andulu. 16Ndidzawabalalitsanso mwa amitundu, amene iwo kapena
makolo ao sanawadziwa; ndipo ndidzatumiza lupanga, liwatsate
mpaka ndawatha.
17Atero Yehova wa makamu, Kumbukirani inu, ndi kuitana akazi
akulira, adze; aitaneni akazi ocenjera, kuti adze; 18afulumire,
atikwezere ife mau a maliro, kuti maso athu agwe misozi, ndi
zikope zathu ziyendetse madzi. 19Pakuti mau a kulira amveka

m'Ziyoni, Tafunkhidwa, tanyazitsidwa, pakuti tasiya dziko, pakuti agwetsa zokhalamo zathu. 20Koma imvani mau a Yehova, akazi inu, khutu lanu lilandire mau a pakamwa pace, phunzitsani ana anu akazi kulira, ndi yense aphunzitse mnzace maliridwe ace. 21Pakuti imfa yakwera m'mazenera athu, yalowa m'nyumba mwathu; kucotsa ana kubwalo, ndi: anyamata kumiseu. 22Nenani, atero Yehova, Mitembo yathu idzagwa ngati ndowe pamunda, ndi monga cipukutu pambuyo pa wakusenga, palibe wocitola. 23Atero Yehova, wanzeru asadzitamandire m'nzeru zace, wamphamvu asadzitamandire m'mphamvu yace, wacuma asadzitamandire m'cuma cace; 24koma wakudzitamandira adzitamandire adzikweze umo, kuti ali wakuzindikira, ndi kundidziwa Ine, kuti ndine Yehova wakucita zokoma mtima, ciweruziro, ndi cilungamo m'dziko lapansi, pakuti m'menemo ndikondwerera, ati. Yehova. 25Taonani, masiku alikudza, ati Yehova, kuti ndidzalanga onse odulidwa m'kusadulidwa kwao; 26Aigupto, ndi Yuda, ndi Edomu, ndi ana a Amoni, ndi a Moabu, ndi onse ometa m'mphepete mwa tsitsi lao, okhala m'cipululu; pakuti amitundu onse ali osadulidwa, ndi nyumba ya Israyeli iri Yosadulidwa m'mtima.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Mofano ndi acabe, Yehova ndiye

1Tamvani mau amene Yehova anena kwa inu, nyumba ya
Israyeli; 2atero Yehova, a Musaphunzire njira ya amitundu,
musaope zizindikiro za m'thambo; pakuti amitundu aziopa
izo. 3Pakuti miyambo ya anthu iri yacabe, pakuti wina adula
mtengo m'nkhalango, nchito ya manja a mmisiri
ndinkhwangwa. 4Aukometsa ndi siliva ndi golidi; aucirikiza ndi
misomali ndi nyundo, kuti usasunthike. 5Mafanowa akunga mtengo
wakanjedza, wosemasema, koma osalankhula; ayenera
awanyamule, pakuti sangathe kuyenda. Musawaope; pakuti
sangathe kucita coipa, mulibenso mwa iwo kucita
cabwino. 6Cifukwa palibe akunga Inu, Yehova; muli wamkuru, ndipo
dzina lanu liri lalikuru ndi lamphamvu, 7Wosaopa Inu ndani, Mfumu
ya amitundu? pakuti kukuopani ndi kwanu; pakuti mwa anzeru
onse a amitundu, ndi m'maufumu ao onse, mulibe akunga
Inu. 8Koma onse pamodzi apulukira ndi kupusa; mtengo ndiwo
cilangizo, copanda pace. 9Abwera ndi siliva wa ku Tarisi,
wosulasula wopyapyala ndi golidi wa ku Ufazi, nchito ya mmisiri
ndi manja a woyenga; zobvala zao ndi nsaru ya madzi ndi yofiirira;
zonsezi ndi nci ito za muomba. 10Koma Yehova ndiye Mulungu
woona; ndiye Mulungu wamoyo, mfumu yamuyaya; pa mkwiyo
wace dziko lapansi lidzanthunthumira, ndi amitundu sangapirire
ukali wace.
11Muzitero nao, milungu imene sinalenga miyamba ndi dziko
lapansi, iyo idzatha ku dziko lapansi, ndi pansi pa miyambayo.
12Iye analenga dziko lapansi ndi mphamvu yace, nakhazikitsa
dziko lapansi ndi nzeru yace, nayala thambo ndi kuzindikira
kwace; 13polankhula Iye, pali unyinji wa madzi m'mwamba, ndipo
akweretsa nkhungu ku malekezero a dziko lapansi, alenga mphezi
idzetse mvula, naturutsa mphepo m'zosungira zace. 14Anthu onse
ali opulukira ndi opanda nzeru; woyenga yense anyazitsidwa ndi
fanizo lace losemasema; pakuti fanizo lace loyenga liri bodza,
mulibe mpweya mwa iwo. 15Ndiwo cabe, ndiwo ciphamaso; pa
nthawi ya kulangidwa kwao adzatha. 16Gawo la Yakobo silifanana
ndi iwo; pakuti iye ndiye analenga zonse; Israyeli ndiye mtundu wa
colowa cace; dzina lace ndi Yehova wa makamu.

Aneneratu kuti adzatengedwa ukapolo

17Nyamula katundu wako, iwe wokhala m'linga. 18Pakuti atero
Yehova, Taonani, ndidzaponya kunja okhala m'dziko ili tsopanoli,
ndi kuwasautsa, kuti azindikire. 19Tsoka ine, ndalaswa! bala langa
lindipweteka; koma ine ndinati, Ndithu bvuto langa ndi ili, ndipirire
nalo. 20Hema wanga waonongeka, zingwe zanga zonse zaduka;
ana anga aturuka mwa ine, palibe iwo; palibenso amene

adzamanga hema wanga, kapena kucinga nsaru zanga, 21Pakuti
abusa apulukira, sanafunsire kwa Yehova; cifukwa cace
sanapindula; zoweta zao zonse zabalalika. 22Mbiri yamveka,
taonani ikudza, ndi phokoso lalikuru lituruka m'dziko la kumpoto,
likacititse midzi ya Yuda bwinja, ndi mbuto ya nkhandwe. 23Inu
Yehova, ndidziwa kuti njira ya munthu siri mwa iye mwini; sikuli
kwa munthu woyenda kulongosola mapazi ace. 24Yehova,
mundilangize, koma ndi ciweruzo; si m'mkwiyo wanu,
mungandithe psiti. 25Tsanulirani ukali wanu pa amitundu
osakudziwani Inu, ndi pa mabanja osaitana dzina lanu; pakuti
anadya Yakobo, inde, anamudya namutha, napasula mokhalamo
mwace.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Za kutyola panganolo

1Mau amene anadza kwa Yeremiya kucokera kwa Yehova,
kuti, 2Imvani mau a pangano ili, nenani kwa anthu a Yuda, ndi
anthu a Yerusalemu; 3ndi kunena kwa iwo, Atero Yehova, Mulungu
wa Aisrayeli: Wotembereredwa ndi munthu wosamvera mau a
pangano ili, 4limene ndinauza makolo anu tsiku lomwe
ndinawaturutsa m'dziko la Aigupto, m'ng'anjo ya citsulo, kuti,
Mverani mau anga, ndi kuwacita, monga mwa zonse zimene
ndikuuzani inu; ndipo mudzakhala anthu anga, ndipo Ine
ndidzakhala Mulungu wanu; 5kuti ndikalimbikitse lumbiro limene
ndinalumbirira makolo anu, ndiwapatse dziko mayenda mkaka ndi
uci, monga lero lomwe. Ndipo ndinayankha, ndi kuti, Amen,
Yehova.
6Ndipo Yehova anati kwa ine, Lalikira mau onsewa m'midzi ya
Yuda, ndi m'miseu ya Yerusalemu, kuti, Tamvani mau a pangano ili,
ndi kuwacita. 7Pakuti ndinatsimikizitsa kwa atate anu tsiku lomwe
ndinawaturutsa iwo ku dziko la Aigupto, mpaka lero lomwe, kuuka
mamawa ndi kutsimikiza, kuti, Mverani mau anga. 8Koma
sanamvera, sanachera khutu lao, koma onse anayenda
m'kuumirira kwa mtima wao woipa; cifukwa cace ndinatengera iwo
mau onse a pangano ili, limene ndinauza iwo kuti acite, koma
sanacita.
9Ndipo Yehova anati kwa ine, Ciwembu caoneka mwa anthu a
Yuda, ndi mwa anthu okhala m'Yerusalemu. 10Abwerera kucitanso
zoipa za makolo ao, amene anakana kumva mau anga; ndipo
atsata milungu yina kuti aitumikire; nyumba ya Israyeli ndi
nyumba ya Yuda zaswa pangano langa limene ndinapangana ndi
makolo ao. 11Cifukwa cace atero Yehova, Taonani, ndidzatengera
pa iwo coipa, cimene sangathe kucipulumuka; ndipo
adzandipfuulira Ine, koma sindidzamvera iwo. 12Ndipo midzi ya
Yuda ndi okhala m'Yerusalemu adzapita nadzapfuulira kwa milungu
imene anaifukizira; koma siidzawapulumutsa konse nthawi ya
nsautso yao. 13Pakuti milungu yako ilingana ndi kucuruka kwa
midzi yako, iwe Yuda; ndi maguwa a nsembe amene mwautsira
camanyazi, alingana ndi kucuruka kwa miseu ya Yerusalemu,
ndiwo maguwa akufukizirapo Baala. 14Cifukwa cace
usawapempherere anthu awa, usawakwezere iwo mfuu, kapena
pemphero, pakuti sindidzamva iwo nthawi imene andipfuulira Ine
m'kusaukakwao.
15Wokondedwa wanga afunanji m'nyumba mwanga, popeza wacita
coipa ndi ambiri, ndipo thupi lopatulika lakucokera iwe? pamene
ucita coipa ukondwera naco. 16Yehova anacha dzina lako, Mtengo
waazitona wauwisi, wokoma wa zipatso zabwino; ndi mau a

phokoso lalikuru wayatsa moto pamenepo, ndipo nthambi zace zatyoka. 17Pakuti Yehova wa makamu, amene anakuoka iwe, wakunenera iwe coipa, cifukwa ca zoipa za nyumba ya Israyeli ndi nyumba ya Yuda, zimene anadzicitira okha pakuutsa mkwiyo wanga m'mene anafukizira Baala.

Ampangira Yeremiya ciwembu

18Ndipo Yehova anandidziwitsa, ndipo ndinadziwa; ndipo wandisonyeza ine macitidwe ao. 19Koma ine ndinanga mwana wa nkhosa wofatsa wotengedwa kukaphedwa; ndipo sindinadziwa kuti anandicitira ine ciwembu, kuti, Tiononge mtengo ndi zipatso zace, timdule iye pa dziko la amoyo, kuti dzina lace lisakumbukikenso. 20Koma, Yehova wa makamu, amene aweruza molungama, pamene ayesa imso ndi mtima, ndikuoneni Inu mulikuwabwezera cilango, pakuti kwa Inu ndaulula mlandu wanga. 21Cifukwa cace atero Yehova za anthu a Anatoti, amene afuna moyo wanga, kuti, Usanenere m'dzina la Yehova, ungafe ndi mkono wathu; 22cifukwa cace atero Yehova wa makamu, Taonani, ndidzalanga iwo; anyamata adzafa ndi lupanga; ana ao amuna ndi akazi adzafa ndi njala; 23ndipo sadzakhala nao otsalira; pakuti ndidzatengera coipa pa anthu a ku Anatoti, caka ca kulangidwa kwao.

©The Bible Society of Malawi, 1992

1Wolungama ndinu, Yehova, pamene nditsutsana nanu mlandu;
pokhapo ndinenane nanu za maweruzo; cifukwa canji ipindula njira
ya oipa? cifukwa canji akhala bwino onyengetsa? 2Inu mwabzyala
iwo, inde, anagwiritsatu mizu; amera, inde, abalatu zipatso; muli
pafupi m'kamwa mwao, muli patari ndi imso zao. 3Koma inu,
Yehova, mundidziwa ine; mundiona ine, muyesa mtima wanga ngati
utani nanu; muwaturutse iwo monga nkhosa za kuphedwa, ndi
kuwakonzeratu tsiku lakuphedwa. 4Dziko lidzalira masiku angati,
nilifota therere la minda yonse? cifukwa ca zoipa za iwo okhalamo,
zithedwa zinyama, ndi mbalame; pakuti iwo anati, Iye sadzaona
citsiriziro cathu. 5Ngati wathamanga pamodzi ndi oyenda pansi,
ndipo iwo anakulemetsa iwe, udzayesana nao akavalo bwanji?
ndipo ngakhale ukhazikika m'dziko lamtendere, udzacita ciani
m'kudzikuza kwa Yordano? 6Pakuti ngakhale abale ako, ndi nyumba
ya atate wako, ngakhale iwo anakunyenga iwe; ngakhale
anakupfuulira iwe; usamvere iwo, ngakhale anena nawe mau
abwino.

Dziko lipasuka, Aneneratu za olipasula

7Ndacokaku nyumba yanga, ndasiya colowa canga; ndapereka
wokondedwa wa mtima wanga m'dzanja la adani. 8Colowa canga
candisandukira mkango wa m'nkhalango; anatsutsana nane ndi
mau ace; cifukwa cace ndinamuda. 9Colowa canga ciri kwa ine
ngati mbalame yamawala-mawala yolusa? kodi mbalame zolusa
zimzinga ndi kudana naye? mukani, musonkhanitse zirombo za
m'thengo, mudze nazo zidye. 10Abusa ambiri aononga munda
wanga wamphesa, apondereza gawo langa, pondikondweretsa
apayesa cipululu copanda kanthu. 11Apayesa bwinja; pandilirira
ine, pokhala bwinja; dziko lonse lasanduka bwinja; cifukwa palibe
munthu wosamalira. 12Akufunkha afika pa mapiri oti se m'cipululu;
pakuti lupanga la Yehova lilusa kuyambira pa mbali yina ya dziko
kufikira ku mbali yina; palibe thupi lokhala ndi mtendere. 13Abzyala
tirigu, asenga minga; adzipweteka, koma osapindula kanthu,
mudzakhala ndi manyazi a zipatso zanu, cifukwa ca mkwiyo
woopsya wa Yehova.

14Atero Yehova ponenera anansi anga onse oipa, amene akhudza
colowa cimene ndalowetsamo anthu anga Israyeli; taonani,
ndidzazula iwo m'dziko lao, ndipo ndidzazula nyumba ya Yuda
pakati pao. 15Ndipo padzakhala kuti nditazula iwo, ndidzabwera,
ndipo ndidzawacitira cisoni; ndipo ndidzabwezanso iwo, yense ku
colowa cace, ndi yense ku dziko lace. 16Ndipo padzakhala kuti,
ngati iwo adzaphunzira mwakhama njira za anthu anga, kulumbira
ndi dzina langa, Pali Yehova; monga anaphunzitsa anthu anga
kulumbira pali Baala; pamenepo ndidzamangitsa mudzi wao pakati

pa anthu anga. 17Koma ngati sakumva, ndidzazula mtundu umene
wa anthu, kuuzula ndi kuuononga, ati Yehova.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Fanizo la mpango wabafuta lifanizira kulangidwa kwao

1Atero Yehova kwa ine, Pita, udzigulire mpango wabafuta,
nudzimangire m'cuuno mwako, usauike m'madzi. 2Ndipo ndinagula
mpango monga mwa mau a Yehova, ndi kubvala m'cuuno
mwanga. 3Ndipo mau a Yehova anadza kwa ine nthawi yaciwiri,
kuti, 4Tenga mpango umene unaugula, umene uli m'cuuno mwako,
nuuke, nupite ku Firate, nuubise m'menemo m'phanga la
m'mwala. 5Ndipo ndinapita, ndinaubisa pa Firate, monga Yehova
anandiuza ine. 6Ndipo panali atapita masiku ambiri, kuti Yehova
anati kwa ine, Uka, pita ku Firate, nukatenge kumeneko mpango
uja, ndinakuuza iwe ukaubise kumeneko. 7Ndipo ndinanka ku
Firate, ndikumba, nditenga mpango m'malo m'mene
ndinaubisamo; ndipo, taonani, mpango unaonongeka, wosayenera
kanthu. 8Ndipo mau a Yehova anadza kwa ine, kuti, 9Yehova atero,
Momwemo ndidzaononga kudzitama kwa Yuda, ndi kudzitama
kwakukuru kwa Yerusalemu. 10Anthu oipa awa, amene akana
kumva mau anga, amene ayenda m'kuumirira kwa mtima wao,
atsata milungu yina kuitumikira, ndi kuigwadira, adzakhala ngati
mpango uwu, wosayenera kanthu. 11Pakuti monga mpango uthina
m'cuuno ca munthu, comweco ndinathinitsa kwa Ine nyumba
yonse ya Israyeli ndi nyumba yonse ya Yuda, ati Yehova, kuti
akhale kwa Ine anthu, ndi dzina, ndi cilemekezo, ndi ulemerero;
koma anakana kumva. 12Cifukwa cace uzinena ndi iwo mau awa:
Atero Yehova, Mulungu wa Israyeli, Matumba onse adzadzazidwa
ndi vinyo; ndipo adzati kwa iwe, Kodi sitidziwitsa bwino kuti
matumba onse adzadzazidwa ndi vinyo? 13Ndipo udzati kwa iwo,
Atero Yehova, Taonani, ndidzadzaza ndi ciledzero onse okhala
m'dziko muno, ngakhale mafumu onse amene akhala pa mpando
wacifumu wa Davide, ndi ansembe, ndi aneneri, ndi onse okhala
m'Yerusalemu. 14Ndipo ndidzaphwanyanitsa wina ndi wina, atate
ndi ana, ati Yehova; sindidzakhala ndi cisoni, sindidzapulumutsa,
sindidzakhala ndi cifundo, cakuti ndisawaononge.
15Tamvani inu, Cherani khutu; musanyade, pakuti Yehova
wanena. 16Lemekezani Yehova Mulungu wanu, kusanade, mapazi
anu asanakhumudwe pa mapiri acizirezire; nimusanayembekeze
kuunika, Ive asanasandutse kuunikaku mthunzi wa imfa, ndi
kukuyesa mdima wa bii. 17Koma ngati simudzamva, moyo wanga
udzalira m'tseri cifukwa ca kunyada kwanu; diso langa lidzalira
kwambiri, lidzagwa misozi, cifukwa zoweta za Yehova zagwidwa
m'nsinga. 18Nenani kwa mfumu ndi kwa amace wa mfumu,
Dzicepetseni, khalani pansi; pakuti zapamtu zanu zagwa, korona
wanu wokoma. 19Midzi ya ku Mwera yatsekedwa, palibe

wotsegulira. Yuda wonse wacotsedwa m'ndende wonsewo,
wacotsedwa m'nsinga.
20Tukulani maso anu, taonani iwo amene acokera kumpoto; ziri kuti
zoweta zinapatsidwa kwa iwe, zoweta zako zokoma? 21Udzanena
ciani pamene adzaika abale ako akuru ako, pakuti iwe wekha
wawalangiza iwo akukana iwe? kodi zowawa sizidzakugwira iwe
monga mkazi wobala? 22Ndipo ngati udzati m'mtima mwako,
Zimenezi zandifikira ine cifukwa ninji? Cifukwa ca coipa cako
cacikuru nsaru zako zoyesa mfula zasanduka mbudulira, ndi
zithende zako zaphwetekwa. 23Kodi angathe Mkusi kusanduliza
khungu lace, kapena nyalugwe maanga ace? pamenepo mungathe
inunso kucita zabwino, inu amene muzolowera kucita
zoipa, 24Cifukwa cace ndidzabalalitsa iwo, monga ziputu zakupita,
ndi mphepo ya kucipululu. 25Ici ndi cagwera cako, gawo la muyeso
wako wa kwa Ine, ati Yehova; cifukwa wandiiwala Ine, ndi
kukhulupirira zonama. 26Cifukwa cace Ine ndidzaonetsa zotopola
mikawo zako, pamaso pako, ndipo manyazi ako
adzaoneka. 27Ndaona zonyansa zako, ndi zigololo zako, ndi
zakumemesa zako, ndi cinyerinyeri ca dama lako, pamapiri ndi
m'munda. Tsoka kwa iwe, Yerusalemu! Sudzayeretsedwa; kodi
zidzatero mpaka liti?

©The Bible Society of Malawi, 1992

Yeremiya apempherera anthu

1Mau a Yehova amene anadza kwa Yeremiya onena za cirala. 2Yuda
alira, ndipo zipata zace zilefuka, zikhala pansi zobvekedwa ndi
zakuda; mpfuu wa Yerusalemu wakwera. 3Akuru ao atuma ang'ono
ao kumadzi; afika kumaenje, osapeza madzi; abwera ndi mitsuko
yao yopanda kanthu; ali ndi manyazi, athedwa nzeru, apfunda
mitu yao. 4Cifukwa ca nthaka yocita ming'aru, pakuti panalibe
mvula padziko, olima ali ndi manyazi, apfunda mitu yao. 5Inde,
nswalanso ya m'thengo ibala nisiya ana ace, cifukwa mulibe
maudzu. 6Mbidzi zinaima pamapiri oti se, zipumira mphepo
wefuwefu ngati ankhandwe; maso ao alema, cifukwa palibe
maudzu.
7Zingakhale zoipa zathu zititsutsa ife, citani Inu cifukwa ca dzina
lanu, Yehova; pakuti zobwerera zathu zacuruka; takucimwirani
Inu. 8Inu, ciyembekezo ca Israyeli, mpulumutsi wace nthawi ya
msauko, bwanji mukhala ngati mlendo m'dziko, ngati
woyendayenda amene apatuka usiku? 9Bwanji mukhala ngati
munthu wodabwa, ngati munthu wamphamvu wosatha
kupulumutsa? koma Inu, Yehova, muli pakati pathu, tichedwa ndi
dzina lanu; musatisiye.

Yehova osamvera pempherolo

10Atero Yehova kwa anthu awa, Comwecoakonda kusocerera;
sanakaniza mapazi ao; cifukwa cace. Yehova sawalandira; tsopano
adzakumbukira coipa cao, nadzalanga zocimwa zao. 11Ndipo
Yehova anati kwa ine, Usapempherere anthu awa
zabwino. 12Pamene asala cakudya, sindidzamva kupfuula kwao;
ndipo pamene apereka nsembe yopsereza, ndi nsembe yaufa
sindidzawalandira; koma ndidzawatha ndi lupanga, ndi cirala, ndi
caola. 13Ndipo ndinati, Ha, Ambuye Yehova! taonani, aneneri ati
kwa iwo, Simudzaona lupanga, simudzakhala ndi cirala; koma
ndidzakupatsani mtendere weniweni mommuno. 14Ndipo Yehova
anati kwa ine, Aneneri anenera zonama m'dzina langa;
sindinatuma iwo, sindinauza iwo, sindinanena nao; anenera kwa
inu masomphenya onama, ndi ula, ndi cinthu cacabe, ndi cinyengo
ca mtima wao. 15Cifukwa cace atero Yehova za aneneri onenera
m'dzina langa, ndipo sindinawatuma, koma ati, Lupanga ndi cirala
sizidzakhala m'dziko muno; ndi lupanga ndi cirala aneneriwo
adzathedwa. 16Ndipo anthu amene adzanenera kwa inu
adzaponyedwa kunja m'miseu ya Yerusalemu cifukwa ca cirala ndi
lupanga; ndipo adzasowa akuwaika, ndi akazi ao, ndi ana ao
amuna ndi akazi; ndipo ndidzatsanulira pa iwo zoipa zao. 17Ndipo
udzati kwa iwo mau awa, Maso anga agwe misozi usana ndi usiku,
asaleke; pakuti namwali mwana wa anthu anga wasweka ndi

kusweka kwakukuru, ndi bala lopweteka kwambiri. 18Ndikaturukira
kumunda, taonani ophedwa ndi lupanga! ndikalowa m'mudzi,
taonani odwala ndi njala pakuti mneneri ndi wansembe
ayendayenda m'dziko osadziwa kanthu.
19Kodi mwakanadi Yuda? kodi mtima wanu wanyansidwa ndi
Ziyoni? bwanji mwatipanda ife, ndipo tiribe kucira? Tinayembekeza
mtendere, koma sizinafike zabwino; tinayembekeza nthawi
yakucira, ndipo taonani mantha! 20Tibvomereza, Yehova,
cisalungamo cathu, ndi coipa ca makolo athu; pakuti takucimwirani
Inu. 21Musatinyoze ife, cifukwa ca dzina lanu; musanyazitse
mpando wacifumu wa ulemerero wanu; mukumbukire musasiye
pangano lanu lopangana ndi ife. 22Mwa zacabe za mitundu ya
anthu ziripo kodi, zimene zingathe kubvumbitsa mvula? Kodi si
ndinu, Yehova, Mulungu wathu? ndipo tidzakudikirani Inu; pakuti
munalenga zonse zimenezi.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Yehova akanadi kumvera

1Ndipo Yehova anati kwa ine, Ngakhale Mose ndi Samueli
akadaima pamaso panga, koma mtima wanga sukadasamalira
anthu awa; muwacotse iwo pamaso panga, aturuke. 2Ndipo
padzakhala, pamene adzati kwa iwe, Titurukire kuti? pamenepo
uziti, Atero Yehova: Amene a kuimfa, anke kuimfa; amene a
kulupanga, anke kulupanga; amene a kunjala, anke kunjala; ndi
amene a kunsinga, anke kunsinga. 3Ndipo ndidzaika pa iwo
mitundu inai, ati Yehova, lupanga lakupha, agaru akung'amba,
mbalame za m'mlengalenga, ndi zirombo zapansi, zakulusa ndi
kuononga. 4Ndipo ndidzawapereka akhale oopsetsa m'maufumu
onse a dziko lapansi, cifukwa ca Manase mwana wa Hezekiya
mfumu ya Yuda, cifukwa ca zija anacita m'Yerusalemu. 5Pakuti
ndani adzakucitira iwe cisoni, Yerusalemu? ndani adzakulirira iwe?
ndani adzapatukira kudzafunsa za mkhalidwe wako? 6Iwe
wandikana Ine, ati Yehova, wabwerera m'mbuyo; cifukwa cace
ndatambasulira dzanja langa pa iwe, ndi kukuononga iwe; ndatopa
ndi kulekerera. 7Ndawakupa ndi mkupo m'zipata za dziko;
ndacotsa ana ao, ndasakaza anthu anga; sanabwerere kuleka njira
zao. 8Amasiye ao andicurukira Ine kopambana mcenga wa
kunyanja; ndatengera wofunkha usana afunkhire mai wao wa
anyamata; ndamgwetsera dzidzidzi kuwawa mtima ndi
mantha. 9Mkazi amene anabala asanu ndi awiri walefuka;
wapereka moyo; dzuwa lace lalowa usana ulipobe; wanyazitsidwa,
wathedwa nzeru; otsala ao ndidzapereka kulupanga pamaso pa
adani ao, ati Yehova.

Kulira kwa Yeremiya, kuyankha kwa Yehova

10Kalanga ine, amai, pakuti mwandibala ine munthu wandeu,
munthu wakutetana nalo dziko lonse lapansi! sindinakongoletsa
paphindu, anthu sanandikongoletsa paphindu; koma iwo onse
anditemberera. 11Yehova anati, Ndithu ndidzakulimbitsira iwe
zabwino; ndithu ndidzapembedzetsa mdani kwa iwe nthawi ya
zoipa ndi nthawi yansautso.
12Kodi angathe munthu kutyola citsulo, citsulo ca kumpoto, ndi
mkuwa? 13Cuma cako ndi zosungidwa zako ndidzazipereka
zifunkhidwe kopanda mtengo wace, icico cidzakugwera cifukwa ca
zocimwa zako zonse, m'malire ako onse. 14Ndipo ndidzawapititsa
iwo pamodzi ndi adani ako ku dziko limene sudziwa iwe; pakuti
moto wayaka m'mkwiyo wanga, umene udzatentha inu.
15Inu Yehova, mudziwa; mundikumbukire ine, mundiyang'anire ine,
mundibwezere cilango pa ondisautsa ine; musandicotse m'cipiriro
canu; dziwani kuti cifukwa ca Inu ndanyozedwa. 16Mau anu
anapezeka, ndipo ndinawadya; mau anu anakhala kwa ine

cikondwero ndi cisangalalo ca mtima wanga; pakuti ndachedwa
dzina lanu, Yehova Mulungu wa makamu. 17Sindinakhala
m'msonkhano wa iwo amene asekera-sekera, ndi kusangalala;
ndinakhala pandekha cifukwa ca dzanja lanu; pakuti mwandidzaza
ndi mkwiyo. 18Kupweteka kwanga kuti cipwetekere bwanji, ndi bala
langa losapoleka, likana kupola? kodi mudzakhala kwa ine ngati
kamtsinje konyenga, ngati madzi omwerera?
19Cifukwa cace atero Yehova, Ukabwerera pamenepo
ndidzakubwezanso, kuti uime pamaso panga; ndipo ukasiyanitsa
ca mtengo wace ndi conyansa, udzakhala ngati m'kamwa
mwanga; ndipo adzabwerera kwa iwe, koma sudzabwerera kwa
iwo. 20Ndidzakuyesa iwe linga lamkuwa la anthu awa; ndipe
adzamenyana ndi iwe, koma iwo sadzakuposa iwe; pakuti Ine ndiri
ndi iwe kuti ndikupulumutse ndi kukulanditsa iwe, ati
Yehova. 21Ndipo ndidzakulanditsa iwe m'dzanja la oipa, ndipo
ndidzakuombola iwe m'dzanja la oopsya.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Aneneratu za kutengedwa ukapolo kwa Israyeli ndi kubweranso kwao

1Ndiponso mau a Mulungu anadza kwa ine, kuti, 2Usatenge mkazi, usakhale ndi ana amuna ndi akazi m'malo muno. 3Pakuti Yehova atero za ana amuna ndi za ana akazi akubadwa m'malo muno, ndi za amai anawabala iwo, ndi za atate ao anawabala iwo m'dziko muno: 4Adzafa ndi imfa zanthenda; sadzaliridwa maliro, sadzaikidwa; adzakhala ngati ndowe panthaka; ndipo adzathedwa lupanga, ndi njala; ndipo mitembo yao idzakhala cakudya ca mbalame za kumlengalenga, ndi zirombo za dziko lapansi. 5Pakuti Yehova atero, Usalowe m'nyumba ya maliro, usanke kukacita maliro ao, kapena kuwalirira; pakuti ndacotsa mtendere wanga pa anthu awa, cifundo ndi nsoni zokoma, ati Yehova. 6Akuru ndi ang'onong'ono adzafa m'dziko muno; sadzaikidwa, anthu sadzacita maliro ao, sadzadziceka, sadzadziyeseza adazi, cifukwa ca iwo; 7anthu sadzawagawira mkate pamaliro, kuti atonthoze mitima yao cifukwa ca akufa, anthu sadzapatsa iwo cikho ca kutonthoza kuti acimwe cifukwa ca atate ao kapena mai wao. 8Usalowe m'nyumba ya madyerero kukhala nao, ndi kudya ndi kumwa. 9Pakuti atero Yehova wa makamu, Mulungu wa Israyeli; Taonani, ndidzaletsa pano, pamaso panu masiku anu, mau akukondwerera ndi mau akusangalala, mau a mkwati ndi mau a mkwatibwi. 10Ndipo padzakhala, pamene udzaonetsa anthu awa mau awa onse, ndipo iwo adzati kwa iwe, Cifukwa cace nciani kuti Yehova watinenera ife coipa cacikuru ici? mphulupulu yathu ndi yanji? cimo lathu lanji limene tacimwira Yehova Mulungu wathu? 11Pamenepo uziti kwa iwo, Cifukwa makolo anu anandisiya Ine, ati Yehova, natsata milungu yina, naitumikira, naigwadira, nandisiya Ine, osasunga cilamulo canga; 12ndipo mwacita zoipa zopambana makolo anu; pakuti, taonani, muyenda yense potsata kuumirira kwa mtima wace woipa, kuti musandimvere Ine; 13cifukwa cace ndidzakuturutsani inu m'dziko muno munke ku dziko limene simunadziwa, kapena inu kapena makolo anu; pamenepo mudzatumikira milungu yina usana ndi usiku, kumene sindidzacitira inu cifundo.

14Cifukwa cace, taonani, masiku adza, ati Yehova, kuti sadzanenanso, Pali Yehova, amene anakweza ana a Israyeli kuwaturutsa m'dziko la Aigupto. 15Koma, Pali Yehova, amene anakweza ana a Israyeli kucokera ku dziko la kumpoto, ndi ku maiko ena kumene anawapitikitsirako; ndipo ndidzawabwezanso ku dziko lao limene ndinapatsa makolo ao. 16Taonani, ndidzaitana akugwira nsomba ambiri, ati Yehova, ndipo adzawagwira iwo, pambuyo pace ndidzaitana osaka nyama ambiri, ndipo adzasaka

iwo m'mapiri onse, ndi pa zitunda zonse, ndiponso m'mapanga a
m'matanthwe. 17Pakuti maso anga ali pa njira zao zonse, sabisika
pa nkhope yanga, mphulupulu yao siibisika pamaso
panga, 18Poyamba ndibwezera mphulupulu yao ndi cimo lao
cowirikiza; cifukwa anaipitsa dziko langa ndi mitembo ya
zodetsedwa zao, nadzaza colowa canga ndi zonyansa zao. 19Inu
Yehova, mphamvu yanga, ndi linga langa, pothawirapo panga tsiku
la msauko, amitundu adzadza kwa Inu kucokera ku malekezero a
dziko lapansi, ndipo adzati, Makolo athu analandira colowa ca
bodza lokha, zopanda pace ndi zinthu zosapindula nazo. 20Kodi
munthu adzadzipangira yekha milungu, imene siiri
milungu? 21Cifukwa cace, taonani, ndidzadziwitsa iwo kamodzi aka,
ndidzawadziwitsa dzanja langa ndi mphamvu yanga; ndipo
adzadziwa kuti dzina langa ndine Yehova.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Cimo la Yuda ndi losafafanizika

1Cimo la Yuda lalembedwa ndi peni lacitsulo, ndi nsonga ya
diamondi; lalembedwa pa colembapo ca m'mtima mwao, ndi pa
nyanga za maguwa a nsembe anu. 2Pokumbukira ana ao maguwa
a nsembe ao ndi zoimiritsa zao ku mitengo yaiwisi ya pa zitunda
zazitari. 3Iwe phiri langa la m'munda, ndidzapereka cuma cako ndi
zosungidwa zako zikafunkhidwe, ndi misanje yako, cifukwa ca
cimo, m'malire ako onse. 4Iwe, iwe wekha, udzaleka pa colowa
cako cimene ndinakupatsa iwe; ndipo ndidzakutumikiritsa adani
ako m'dziko limene sulidziwa; pakuti wakoleza moto m'mkwiyo
wanga umene udzatentha ku nthawi zamuyaya.

Anthu azikhulupirira Yehova yekha

5Atero Yehova: Wotembereredwa munthu amene akhulupirira
munthu, natama mkono wanyama, nucoka kwa Yehova mtima
wace. 6Ndipo adzakhala ngati tsanya la m'cipululu, ndipo saona
pamene cifika cabwino; koma adzakhala m'malo oumitsa
m'cipululu, dziko lacikungu lopanda anthu. 7Wodala munthu amene
akhulupirira Yehova, amene cikhulupiriro cace ndi Yehova. 8Ndipo
adzakhala ngati mtengo wooka kuti madzi, wotambalitsa mizu
yace pamtsinje, wosaopa pofika nyengo yadzuwa, koma tsamba
lace likhala laliwisi; ndipo subvutika cakaca cirala, suleka kubala
zipatso. 9Mtima ndiwo wonyenga koposa, ndi wosaciritsika, ndani
angathe kuudziwa? 10Ine Yehova ndisanthula mtima, ndiyesa imso,
kuti ndimpatse munthu yense monga mwa njira zace, monga
zipatso za nchito zace. 11Monga nkhwali iumatira pa mazira amene
sinaikira, momwemo iye amene asonkhanitsa cuma, koma
mosalungama; pakati pa masiku ace cidzamsiya iye, ndipo pa
citsirizo adzakhala wopusa.
12Malo opatulika athu ndiwo mpando wacifumu wa ulemerero,
wokhazikika pamsanje ciyambire. 13Inu Yehova, ciyembekezo ca
Israyeli, onse amene akukusiyani Inu adzakhala ndi manyazi; onse
ondicokera Ine adzalembedwa m'dothi, cifukwa asiya Yehova,
kasupe wa madzi amoyo. 14Mundiciritse ine, Yehova, ndipo
ndidzaciritsidwa; mundipulumutse ine, ndipo ndidzapulumutsidwa;
pakuti cilemekezo canga ndinu. 15Taonani, ati kwa ine, Mau a
Yehova ali kuti? adze tsopano. 16Koma ine, pokhala mbusa
sindinafulumira kucokerako kuti ndikutsateni Inu; sindinakhumba
tsiku la tsoka; Inu mudziwa, cimene cinaturuka pa milomo yanga
cinali pamaso panu. 17Musakhale wondiopsetsa ine; ndinu
pothawira panga tsiku la coipa. 18Iwo akhale ndi manyazi amene
andisautsa ine, koma ine ndisakhale ndi manyazi; aopsedwe iwo,
koma ndisaopsedwe ine; muwatengere iwo tsiku la coipa,
muwaononge ndi cionongeko cowirikiza.

Za kusunga dzuwa la Sabata

19Yehova anatero kwa ine: Pita, nuime m'cipata ca ana a anthu,
m'mene alowamo mafumu a Yuda, ndi m'mene aturukamo, ndi
m'zipata zonse za Yerusalemu; 20ndipo uziti kwa iwo, Tamvani mau
a Yehova, inu mafumu a Yuda, ndi Ayuda onse, ndi onse okhala
m'Yerusalemu, amene alowa pa zipatazi; 21atero Yehova:
Tadziyang'anirani nokha, musanyamule katundu tsiku la Sabata,
musalowe naye pa zipata za Yerusalemu; 22musaturutse katundu
m'nyumba zanu tsiku la Sabata, musagwire nchito iri onse; koma
mupatule tsiku la Sabata, monga ndinauza makolo anu; 23koma
sanamvera, sanachera khutu lao, koma anaumitsa khosi lao, kuti
asamve, asalandire langizo. 24Ndipo padzakhala, ngati mu
ndimveretsa Ine, ati Yehova, kuti musalowetse katundu pa zipata
za mudzi uwu tsiku la Sabata, koma mupatule tsiku la Sabata,
osagwira nchito m'menemo; 25pamenepo padzalowa pa zipata za
mudzi uwu mafumu ndi akuru okhala pa mpando wacifumu wa
Davide, okwera pa magareta ndi akavalo, iwo, ndi akuru ao, anthu
a Yuda, ndi okhala m'Yerusalemu; ndipo mudzi uwu udzakhala ku
nthawi zamuyaya. 26Ndipo adzacokera ku midzi ya Yuda, ndi ku
malo akuzungulira Yerusalemu, ndi ku dziko la Benjamini, ndi
kucidikha, ndi kumapiri, ndi ku Mwela, ndi kudza nazo nsembe
zopsereza, ndi nsembe zophera, ndi nsembe zaufa, ndi zonunkhira,
ndi kudza nazo zamiyamikiro, ku nyumba ya Yehova. 27Koma ngati
simudzamvera Ine kulipatula tsiku la Sabata, kusanyamula
katundu ndi kulowa pa zipata za Yerusalemu tsiku la Sabata;
pamenepo ndidzayatsa moto m'zipata zacezo, ndipo udzatha
zinyumba za Yerusalemu, osazimidwanso.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Mbiya ya woumba. Anthu osalapa

1Mau amene anadza kwa Yeremiya kucokera kwa Yehova,
kuti, 2Tauka, tatsikira ku nyumba ya woumba, pamenepo
ndidzakumvetsa mau anga. 3Ndipo ndinatsikira ku nyumba ya
woumba, ndipo, taonani, anaumba nchito yace ndi njinga. 4Ndipo
pamene mbiya alikulumba ndi dothi inaonongeka m'dzanja la
woumba, anaiumbanso mbiya yina, monga kunamkomera woumba
kulumba.
5Ndipo mau a Yehova anadza kwa ine, kuti, 6Nyumba ya Israyeli
inu, kodi sindingathe kucita ndi inu monga woumba uyu? ati
Yehova. Taonani, monga dothi m'dzanja la woumba, momwemo inu
m'dzanja langa, nyumba ya Israyeli. 7Mphindi imene ndidzanena
za mtundu wa anthu, kapena za ufumu, kuti ndizule ndi kupasula
ndi kuononga; 8ngati mtundu umene, ndaunenera, udzatembenuka
kuleka coipa cao, ndidzaleka coipaco ndidati ndiwacitire. 9Ndipo
mphindi imene ndikanenera mtundu, ndi ufumu, kuti ndimangitse
mudzi wace ndi kuuoka; 10koma ukacita coipa pamaso panga,
osamvera mau anga, pamenepo ndidzaleka cabwinoco, ndidati
ndiwacitire. 11Tsopano nenatu kwa anthu a Yuda, ndi kwa okhala
m'Yerusalemu, kuti, Atero Yehova: Taonani, Ine ndipangira inu
coipa, ndilingalira inu kanthu kakucitira inu coipa; mubwerere
tsono inu nonse, yense ku njira yace yoipa, nimukonze njira zanu
ndi macitidwe anu. 12Koma iwo ati, Palibe ciyembekezero; pakuti
ife tidzatsata zilingaliro zathu, ndipo tidzacita yense monga mwa
kuuma kwa mtima wacewoipa.
13Cifukwa cace atero Yehova; Funsanitu m'mitundu, ndani wamva
zotero; namwali wa Israyeli wacita cinthu coopsetsa
kwambiri. 14Kodi matalala a Lebano adzalephera pa mwala wa
m'munda? kodi adzaphwa madzi ozizira otsika kutari? 15Pakun
anthu anga andiiwala Ine, afukizira zopanda pace; apunthwitsa iwo
m'njira zao, m'njira zakale kuti ayende m'njira za m'mbali, m'njira
yosatundumuka; 16kuti aliyese dziko lao likhale lodabwitsa, ndi:
kutsonya citsonyere; yense wakupitapo adzadabwa, ndi kupukusa
mutu wace. 17Ndidzamwazamwaza iwo monga ndi mphepo ya
kum'mawa pamaso pa adani; ndidzayang'anira pamsana pao, si
nkhope yao, tsiku la tsoka lao.
18Ndipo iwo anati, Tiyeni, tilingalire Yeremiya comcitira coipa;
pakuti cilamulo sicidzathera wansembe, kapena uphungu wanzeru,
kapena mau mneneri. Tiyeni, timpande iye ndi lilime, tisamvere iye
mau ace ali onse.
19Mundimvere ine, Yehova, mumve mau a iwo akulimbana ndi
ine. 20Kodi coipa cibwezedwe pa cabwino? pakuti akumbira moyo
wanga dzenje, Mukumbukire kuti ndinaima pamaso panu

kuwanenera zabwino, kuwacotsera iwo ukali wanu. 21Cifukwa cace
mupereke ana ao kunjala, mupereke iwo ku mphamvu ya lupanga;
akazi ao akhale opanda ana, ndi amasiye; amuna ao aphedwe ndi
imfa, ndi anyamata ao apandidwe ndi lupanga kunkhondo. 22Mpfuu
umvekedwe m'nyumba zao, pamene muwatengera khamu la
nkhondo dzidzidzi; pakuti akumba dzenje lakundigwira ine,
anabisira mapazi anga misampha. 23Koma, Yehova, mudziwa
uphungu wao wonse wakundinenera ine kundipha ine;
musakhulukire mphulupulu yao, musafafanize cimo lao pamaso
panu; apunthwitsidwe pamaso panu; mucite nao m'nthawi ya
mkwiyo wanu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Nsupa ya woumba isweka, Yerusalemu apasuka

1Atero Yehova, Pita, nugule nsupa ya woumba, nutenge akuru a
anthu, ndi akuru a ansembe; 2nuturukire ku cigwa ca mwana wace
wa Hinomu, cimene ciri pa khomo la cipata ca mapale, nulalikire
kumeneko mau amene ndidzakuuza iwe; 3nuti, Tamvani mau a
Yehova, inu mafumu a Yuda, ndi okhala m'Yerusalemu; Yehova wa
makamu, Mulungu wa Israyeli atero, Taonani, ndidzatengera malo
ano coipa, cimene ali yense adzacimva, makutu ace adzacita
woo. 4Cifukwa andisiya Ine, nayesa malo ano acilendo, nafukizira
m'menemo milungu yina, imene sanaidziwa, iwowa, ndi makolo ao
ndi mafumu a Yuda: nadzaza malo ano ndi mwazi wa
osacimwa; 5namanga misanje ya Baala, kuti apsereze ana ao
m'menemo nsembe zopsereza za Baala, cimene sindinawauza,
sindinacinena, sicinalowa m'mtima mwanga; 6cifukwa cace,
taonani, masiku adza, ati Yehova kuti pamalo pano
sipadzachedwanso Tofeti, kapena Cigwa ca mwana wace wa
Hinomu, koma Cigwa Cophera anthu. 7Ndipo ndidzataya uphungu
wa Yuda ndi wa Yerusalemu m'malo ano; ndipo ndidzagwetsa iwo
ndi lupanga pamaso pa adani ao, ndi pa dzanja la iwo amene
afuna moyo wao; mitembo yao ndidzapatsa ikhale cakudya ca
mbalame za m'mlengalenga, ndi ca zirombo za dziko
lapansi. 8Ndipo ndidzayesa mudziwu codabwitsa, ndi cotsonyetsa;
onse amene adzapitapo adzadabwa ndi kutsonya cifukwa ca
zopanda pace zonse. 9Ndipo ndidzadyetsa iwo mnofu wa ana ao
amuna ndi akazi, ndipo adzadya yense mnofu wa mbale wace,
m'nkhondo yozinga ndi m'kupsinjikako, kumene adani ao, ndi iwo
akufuna moyo wao, adzapsinja iwo nako. 10Pamenepo uziphwanya
nsupa pamaso pa anthu otsagana ndi iwe, 11nuziti kwa iwo, Yehova
wa makamu atero: Comweco ndidzaphwanya anthu awa ndi mudzi
uwu, monga aphwanya mbiya ya woumba, imene sangathe
kulumbanso, ndipo adzaika maliro m'Tofeti, mpaka mulibe malo
akuikamo. 12Ndidzatero ndi malo ano, ati Yehova, ndi okhalamo,
kusanduliza mudzi uwu ngati Tofeti; 13ndi nyumba za Yerusalemu,
ndi nyumba za mafumu a Yuda, zimene ziipitsidwa, zidzanga malo
a Tofeti, ndizo nyumba zonse anafukizira khamu lonse la
kumwamba pa matsindwi ao, ndi kuithirira milungu yina nsembe
zothira.
14Pamenepo Yeremiya anadza kucokera ku Tofeti, kumene Yehova
anamtuma iye kuti anenere; ndipo anaima m'bwalo la nyumba ya
Yehova, nati kwa anthu onse: 15Yehova wa makamu, Mulungu wa
Israyeli atero, Taonani, ndidzatengera mudzi uwu ndi midzi yace
yonse coipa conse cimene ndaunenera; cifukwa anaumitsa khosi
lao, kuti asamve mau anga.

Pasuri wansembe apanda Yeremiya, nammanga m'kaidi

1Ndipo Pasuri mwana wace wa Imeri wansembe, amene anali
kapitao wamkuru m'nyumba ya Yehova, anamva Yeremiya
alikunenera zimenezi. 2Ndipo Pasuri anampanda Yeremiya
mneneriyo, namuika matangadza amene anali m'cipata ca
kumtunda ca Benjamini, cimene cinali ku nyumba ya
Yehova. 3Ndipo panali m'mawa mwace, kuti Pasuri anaturutsa
Yeremiya m'matangadzamo. Ndipo Yeremiya anati kwa iye, Yehova
sanacha dzina lako Pasuri, koma Magorimisabibu. 4Pakuti Yehova
atero, Taonani, ndidzakuyesa iwe coopsa ca kwa iwe mwini, ndi
kwa abale ako onse; ndipo iwo adzagwa ndi lupanga la adani ao,
ndipo maso ako adzaona; ndipo ndidzapereka Ayuda onse
m'dzanja la mfumu ya ku Babulo, ndipo iye adzawatengera iwo
am'nsinga ku Babulo, nadzawapha ndi lupanga, 5Ndiponso
ndidzapereka cuma conse ca mudzi uwu, ndi zaphindu zace zonse,
ndi zinthu zace zonse za mtengo wace, inde, zolemera zonse za
mafumu a Yuda ndidzapereka m'manja mwa adani ao, amene
adzazifunkha, nadzazitenga kunka nazo ku Babulo. 6Ndipo iwe,
Pasuri, ndi onse okhala m'nyumba mwako mudzanka kundende;
ndipo udzafika ku Babulo, ndi pamenepo udzafa, ndi pamenepo
udzaikidwa, iwe, ndi mabwenzi ako onse, amene unawanenera
mabodza.
7Yehova, mwandikopa ine, ndipo ndinakopedwa; muli ndi
mphamvu koposa ine, ndipo mwalakika; ine ndikhala coseketsa
dzuwa lonse, lonse andiseka. 8Pakuti pali ponse ndinena,
ndipfuula; ndipfuula, Ciwawa ndi cofunkha; pakuti mau a Mulungu
ayesedwa kwa ine citonzo, ndi coseketsa, dzuwa lonse. 9Ndipo
ngati nditi, Sindidzamchula Iye, sindidzanenanso m'dzina lace,
pamenepo m'mtima mwanga muli ngati moto wotentha
wotsekedwa m'mafupa anga, ndipo ndalema ndi kupirira,
sindingathe kupiriranso. 10Pakuti ndamva kugogodera kwa ambiri,
mantha pozungulira ponse. Neneza, ndipo tidzamneneza iye, ati
atsamwali anga onse, amene ayang'anira kutsimphina kwanga;
kapena adzakopedwa, ndipo ife tidzamlaka iye, ndipo
tidzambwezera cilango. 11Koma Yehova ali ndi ine ngati
wamphamvu ndi woopsya; cifukwa cace ondisautsa adzapunthwa,
sadzandilala; adzakhala ndi manyazi ambiri, cifukwa sanacita
canzeru, ngakhale ndi kunyazitsa kwamuyaya kumene
sikudzaiwalika. 12Koma, Inu Yehova wa makamu, amene muyesa
olungama, amene muona imso ndi mtima, mundionetse ine
kubwezera cilango kwanu pa iwo; pakuti kwa inu ndaululira mlandu

wanga. 13Muyimbire Yehova, mulemekeze Yehova; pakuti
walanditsa moyo wa aumphawi m'dzanja la ocita zoipa.
14Litembereredwe tsiku limene ndinabadwa; lisadalitsike tsiku
limene amai wanga anandibala ine. 15Atembereredwe munthu
amene anatengera mau kwa atate wanga, kuti, Mwana
wamwamuna anakubadwira iwe; ndi kumsekeretsatu
iye. 16Munthuyo akhale ngati midzi imene Yehova anapasula,
osalekerera; amve mpfuu mamawa, ndi mkuwo pausana; 17cifukwa
sanandipha ine m'mimba; kuti mai wanga akhale manda anga, ndi
mimba yace yaikuru nthawi zonse. 18Cifukwa canji ndinaturuka
m'mimba kuti ndione kutopa ndi kulira, kuti masiku anga athe ndi
manyazi?

©The Bible Society of Malawi, 1992

Kufunsira kwa Zedekiya, kuyankha kwa Yeremiya

1Mau amene anadza kwa Yeremiya kucokera kwa Yehova, pamene
Zedekiya mfumu anatuma kwa iye Pasuri mwana wa Malikiya, ndi
Zefaniya mwana wace wa Maseya wansembe, akati, 2Titunsirenitu
ife kwa Yehova; pakuti Nebukadirezara mfumu wa ku Babulo
atithira ife nkhondo; kapena Yehova adzaticitira ife monga mwa
nchito zace zolapitsa, kuti aticokere.
3Ndipo Yeremiya anati kwa iwo, Muzitero kwa Zedekiya: 4Yehova,
Mulungu wa Israyeli atero, Taonani, ndidzabweza zida za nkhondo
zimene ziri m'manja anu, zimene mumenyana nazo ndi mfumu ya
ku Babulo, ndi Akasidi akuzinga inu, kunja kwa malinga, ndipo
ndidzazisonkhanitsa pakati pa mudzi uwu. 5Ndipo Ine mwini
ndidzamenyana ndi inu ndi dzanja lotambasuka ndi mkono
wamphamvu, m'mkwiyo, ndi m'kupsya mtima, ndi m'ukali
waukuru. 6Ndipo ndidzakantha okhalamo m'mudzi uwu, anthu ndi
nyama, adzafa ndi caola cacikuru, 7Ndipo pambuyo pace, ati
Yehova, ndidzapereka Zedekiya mfumu ya Yuda, ndi atumiki ace,
ndi anthu, ngakhale a m'mudzi uwu amene asiyidwa ndi caola, ndi
lupanga, ndi njala, m'dzanja la Nebukadirezara mfumu ya ku
Babulo, ndi m'dzanja la adani ao, ndi m'dzanja la amene afuna
moyo wao; ndipo adzawakantha ndi lupanga lakuthwa; osawaleka,
osacita cisoni, osacita cifundo. 8Ndipo uziti kwa anthu awa, Yehova
atero, Taonani, ndaika pamaso panu njira ya moyo ndi njira ya
imfa. 9Iye amene akhala m'mudzi uwu adzafa ndi lupanga, ndi
njala, ndi caola; koma iye amene aturuka, napandukira kwa Akasidi
akuzinga inu, adzakhala ndi moyo, ndipo moyo wace udzapatsidwa
kwa iye ngati cofunkha. 10Pakuti ndaika nkhope yanga pa mudzi
uwu ndiucitire coipa, si cabwino, ati Yehova; ndipo udzapatsidwa
m'dzanja la mfumu ya ku Babulo, ndipo iye adzautentha ndi moto.

Aneneratu motsutsa mbumba yacifumu ya Yuda

11Ndipo za nyumba ya mfumu ya Yuda, tamvani mau a
Yehova: 12Nyumba ya Davide iwe, Yehova atero, Cita ciweruzo
m'mawa, ndi kumlanditsa amene afunkhidwa m'dzanja la
wosautsa, kungaturuke kupsa mtima kwanga ngati moto, ndi
kutentha kosazimika, cifukwa ca nchito zanu zoipa, 13Taonani, Ine
ndine mdani wako, iwe wokhala m'cigwa, ndi pa thanthwe la
m'cidikha, ati Yehova; inu amene muti, Ndani adzatsikira
kumenyana ndi ife? ndani adzalowa m'zokhalamo zathu? 14Ndipo
ndidzakulangani inu monga mwa cipatso ca nchito zanu, ati
Yehova; ndipo ndidzayatsa moto m'nkhalango mwace, ndipo
udzatha zonse zomzungulira iye.

©The Bible Society of Malawi, 1992

1Yehova atero: Tsikira ku nyumba ya mfumu ya Yuda, ndi kunena komweko mau awa, 2ndi kuti, Tamvani mau a Yehova, Inu mfumu ya Yuda, amene mukhala pa mpando wa Davide, inu, ndi atumiki anu, ndi anthu anu amene alowa pa zipata izi. 3Yehova atero: Citani ciweruzo ndi cilungamo, landitsani ofunkhidwa m'dzanja la wosautsa; musacite coipa, musamcitire mlendo ciwawa, kapena ana amasiye, kapena akazi amasiye, musakhetse mwazi wosacimwa pamalo pano. 4Pakuti ngati mudzacitadi ici pamenepo, padzalowa pa zipata za nyumba iyi mafumu okhala pa mpando wacifumu wa Davide, okwera m'magareta ndi pa akavalo, iye, ndi atumiki ace, ndi anthu ace. 5Koma ngati simudzamva mau amenewa, Ine ndilumbira, pali Ine mwini, ati Yehova, nyumba iyi idzakhala yabwinja. 6Pakuti Yehova atero za nyumba ya mfumu ya Yuda: Ndikuyesa iwe Gileadi, ndi mutu wa Lebano; koma ndidzakuyesa iwe cipululu, ndi midzi yosakhalamo anthu. 7Ndipo ndidzakupangiratu iwe opasula, yense ndi zida zace; ndipo adzadula mikungudza yako yosankhika nadzaiponya m'moto. 8Ndipo amitundu ambiri adzapita pa mudzi uwu, nadzati yense kwa mnzace, Yehova anatero nao mudzi waukuru uwu cifukwa ninji? 9Ndipo adza yankha, Cifukwa anasiya pangano la Yehova Mulungu wao, ndi kugwadira milungu yina, ndi kuitumikira.
10Musamlirire wakufa, musacite maliro ace; koma mumliritse iye amene amuka, pakuti sadzabweranso, kapena kuonanso dziko la kwao. 11Pakuti Yehova atero za Salumu mwana wace wa Yosiya, mfumu ya Yuda, amene analamulira m'malo mwace mwa Yosiya atate wace, amene anaturuka m'malo muno: Sadzabweranso kuno nthawi iri yonse; 12koma kumene anamtengera iye ndende, kumeneko adzafa, ndipo sadzaonanso dziko ili.
13Tsoka iye amene amanga nyumba yace ndi cisalungamo, ndi zipinda zapamwamba ndi cosaweruza bwino; amene agwiritsa mnzace nchito osamlipira, osampatsa mphotho yace; 14amene ati, Ndidzadzimangira ndekha nyumba yotakata ndi zipinda zapamwamba zazikuru, nadziboolera mazenera; nabvundima chindwi lam'kati ndi mikungudza, naipaka ndi utoto wofiira. 15Kodi udzakhala mfumu, cifukwa iwe uyesa kuposa ena ndi mikungudza? Kodi atate wako sanadya ndi kumwa, ndi kuweruza molungama? kumeneko kunamkomera. 16Iye anaweruza mlandu wa aumphawi ndi osowa; kumeneko kunali kwabwino. Kodi kumeneko si kundidziwa Ine? ati Ambuye. 17Koma maso ako ndi mtima wako sizisamalira kanthu koma kusirira, ndi kukhetsa mwazi wosacimwa, ndi kusautsa, ndi zaciwawa, kuti uzicite. 18Cifukwa cace Yehova atero za Yehoyakimu mwana wace wa Yosiya, mfumu ya Yuda: Sadzamlira iye, kuti, Kalanga ine mbale wanga! kapena, Kalanga

ine mlongo wanga! Sadzamlira, kuti, Kalanga ine mbuye! kapena,
Kalanga ine ulemerero wace! 19Adzamuika monga kuika buru,
adzamkoka nadzamponya kunja kwa zipata za Yerusalemu.
20Kwera ku Lebano, nupfuule; kweza mau ako m'Basani; nupfuule
m'Abarimu; pakuti mabwenzi ako onse atha, 21Ndinanena ndi iwe
m'phindu lako; koma unati, Sindidzamva. Awa ndi makhalidwe ako
kuyambira ubwana wako, kuti sudamvera mau anga, 22Mphepo
idzadyetsa abusa ako onse, ndipo mabwenzi ako adzalowa
m'ndende; ntheradi udzakhala ndi manyazi ndi kunyazitsidwa
cifukwa ca coipa cako conse. 23Iwe wokhala m'Lebano, womanga
cisa cako m'mikungudza, udzacitidwa cisoni cacikuru nanga
pamene mapweteko adzadza kwa iwe, monga mkazi
alinkudwala! 24Pali ine, ati Yehova, ngakhale Koniya mwana wace
wa Yehoyakimu mfumu ya Yuda akadakhala mphete ya pa dzanja
langa lamanja, ndikadacotsa iwe kumeneko; 25ndipo
ndidzakupereka iwe m'dzanja la iwo amene afuna moyo wako,
m'dzanja la iwo: amene uwaopa, m'dzanja la Nebukadirezara
mfumu ya ku Babulo, m'dzanja la Akasidi. 26Ndipo ndidzakuturutsa
iwe, ndi mai wako wakubala iwe, kulowa m'dziko lina, limene
sunabadwiramo; m'menemo udzafa. 27Koma kudziko kumene
moyo wao ukhumba kubwerera, kumeneko sadzabwerako. 28Kodi
munthu uyu Koniya ndiye mbiya yopepuka yosweka? Kodi ndiye
mbiya yosakondweretsa? cifukwa canji aturutsidwa iye, ndi mbeu
zace, ndi kuponyedwa m'dziko limene salidziwa? 29Iwe dziko, dziko,
dziko lapansi, tamvera mau a Yehova. 30Atero Yehova, Lembani
munthu uyu wopanda ana, munthu wosaona phindu masiku ace;
pakuti palibe munthu wa mbeu zace adzaona phindu, ndi kukhala
pa mpando wacifumu wa Davide, ndi kulamuliranso m'Yuda.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Mau akutsutsa abusa osakhulupirika

1Tsoka abusa amene athetsa nabalalitsa nkhosa za busa langa! ati
Yehova. 2Cifukwa cace atero Yehova, Mulungu wa Israyeli,
ponenera abusa amene adyetsa anthu anga: Mwabalalitsa zoweta
zanga, ndi kuzipitikitsa, ndipo simunazizonda; taonani,
ndidzakusenzani inu kuipa kwa nchito zanu, ati Yehova. 3Ndipo
ndidzasonkhanitsa zotsala za zoweta zanga za m'maiko onse
m'mene ndinazipitikitsiramo, ndipo ndidzazitengeranso ku makola
ao; ndipo zidzabalana ndi kucuruka. 4Ndipo ndidzaziikira abusa
amene adzazidyetsa; sadzaopanso, kapena kutenga nkhawa,
sipadzasowa mmodzi yense, ati Yehova.

Mphukira wa Davide

5Taonani, masiku alinkudza, ati Yehova, ndidzamuukitsira Davide
Mphukira wolungama, ndipo Iye adzakhala Mfumu, adzacita
mwanzeru, nadzacita ciweruzo ndi cilungamo m'dziko lino. 6Masiku
ace Yuda adzapulumutsidwa, ndipo Israyeli adzakhala mokhazikika,
dzina lace adzachedwa nalo, ndilo Yehova ndiye cilungamo
cathu. 7Cifukwa cace, taonani, masiku alinkudza, ati Yehova,
amene sadzatinso, Pali Yehova, amene anakweza ana a Israyeli
kuwaturutsa m'dziko la Aigupto; 8koma, Pali Yehova, amene
anakweza ndi kutsogolera mbeu za nyumba ya Israyeli
kuwaturutsa m'dziko la kumpoto, ndi ku maiko onse kumene
ndinawapitikitsirako, ndipo adzakhala m'dziko lao.

Mau akutsutsa aneneri onama

9Za aneneri. Mtima wanga usweka m'kati mwanga, mafupa anga
onse anthunthumira; ndinga munthu woledzera, ngati munthu
amene vinyo anamposa; cifukwa ca Yehova, ndi cifukwa ca mau
ace opatulika. 10Pakuti dziko ladzala ndi acigololo; pakuti cifukwa
ca temberero dziko lilira, mabusa a kucipululu auma; kuyenda
kwao kuli koipa, ndi mphamvu yao siiri yabwino. 11Pakuti mneneri
ndi wansembe onse awiri adetsedwa; inde, m'nyumba yanga
ndapeza zoipa zao, ati Yehova. 12Cifukwa cace njira yao idzakhala
kwa iwo yonga malo akuterereka m'mdima; adzacotsedwa,
nadzagwa momwemo; pakuti ndidzawatengera zoipa, caka ca
kulangidwa kwao, ati Yehova. 13Ndipo ndinaona kupusa mwa
aneneri a ku Samariya; anenera za Baala, nasokeretsa anthu anga
Israyeli. 14Mwa aneneri a ku Yerusalemu ndinaona cinthu
coopsetsa; acita cigololo, ayenda monama, alimbitsa manja a ocita
zoipa, ndipo palibe wobwerera kuleka zoipa zace; onse akhala kwa
Ine ngati Sodomu, ndi okhalamo ace ngati Gomora.
15Cifukwa cace Yehova wa makamu atero za aneneri: Taonani,
ndidzadyetsa iwo cowawa, ndidzamwetsa iwo madzi andulu; pakuti
kwa aneneri a ku Yerusalemu kuipitsa kwaturukira kunka ku dziko

lonse. 16Yehova wa makamu atero, Musamvere mau a aneneri amene anenera kwa inu; akuphunzitsani zacabe; anena masomphenya a mtima wao, si a m'kamwa mwa Yehova. 17Anena cinenere kwa iwo akundinyoza Ine, ati Yehova, Mudzakhala ndi mtendere; ndipo kwa yense amene ayenda m'kuumirira kwa mtima wace amati, Palibe coipa cidzagwera inu. 18Pakuti ndani waima m'upo wa Yehova, kuti aone namve mau ace? ndani wazindikira mau anga, nawamva? 19Taonani, cimphepo ca Yehova, kupsa mtima kwace, kwaturuka, inde cimphepo cozungulira; cidzagwa pamutu pa woipa. 20Mkwiyo wa Yehova sudzabwerera, mpaka atacita, mpaka atatha maganizo a mtima wace; masiku otsiriza mudzacidziwa bwino. 21Sindinatuma aneneri awa, koma anathamanga; sindinanena ndi iwo, koma ananenera. 22Koma akadaima m'upo wanga, akadamvetsa anthu anga mau anga, akadatembenuza iwo ku njira yao yoipa, ndi ku coipa ca nchito zao. 23Kodi ndine Mulungu wa pafupi, ati Yehova, si Mulungu wa patari? 24Kodi munthu angathe kubisala mobisika kuti ndisamuone iye? ati Yehova. Kodi Ine sindidzala kumwamba ndi dziko lapansi? ati Yehova. 25Ndamva conena aneneri, amene anenera zonama m'dzina langa, kuti, Ndalota, ndalota. 26Ici cidzakhala masiku angati m'mtima mwa aneneri amene anenera zonama; ndiwo aneneri a cinyengo ca mtima wao? 27amene aganizira kuti adzaiwalitsa anthu anga dzina langa, ndi maloto ao amene anena munthu yense kwa mnansi wace, monga makolo ao anaiwala dzina limene ndimcha nalo Baala. 28Mneneri wokhala ndi loto, anene loto lace; ndi iye amene ali ndi mau anga, anene mau anga mokhulupirika. Kodi phesi ndi ciani polinganiza ndi tirigu? ati Yehova. 29Kodi mau anga safanafana ndi moto? ati Yehova, ndi kufanafana ndi nyundo imene iphwanya mwala? 30Cifukwa cace, taonani, Ine ndidana ndi aneneri, ati Yehova, amene amaba mau anga, yense kumbera mnansi wace. 31Taonani, Ine ndidana ndi aneneri, ati Yehova, amene acita ndi malilime ao, ndi kuti, Ati Iye. 32Taonani, Ine ndidana ndi amene anenera maloto onama, ndi kuwafotokoza ndi kusokeretsa anthu anga ndi zonama zao, ndi matukutuku ao acabe; koma Ine sindinatuma iwo, sindinauza iwo; sadzapindulira konse anthu awa, ati Yehova. 33Ndipo pamene anthu awa, kapena mneneri, kapena wansembe, adzakufunsa iwe, kuti, Katundu wa Yehova ndi ciani? pamenepo uziti kwa iwo, Katundu wanji? Ndidzakucotsani inu, ati Yehova. 34Koma za mneneri, ndi wansembe, ndi anthu, amene adzati, Katundu wa Yehova, ndidzamlanga munthuyo ndi nyumba yace. 35Mudzatero yense kwa mnansi wace, ndi yense kwa mbale wace, Yehova wayankha ciani? ndipo Yehova wanena ciani? 36Ndipo katundu wa Yehova simudzachulanso konse; pakuti

mau a munthu adzakhala katundu wace; pakuti mwasokoneza mau
a Mulungu wamoyo, Yehova wa makamu, Mulungu
wathu. 37Uzitero kwa mneneri, Yehova wakuyankha ciani? ndipo
Yehova wanenanji? 38Koma ngati muti, Katundu wa Yehova,
cifukwa cace Yehova atero: Cifukwa muti mau awa, Katundu wa
Yehova, ndipo ndatuma kwa inu, kuti, Musati, Katundu wa
Yehova; 39cifukwa cace, taonani, ndidzakuiwalani inu konse, ndipo
ndidzakucotsani, ndi mudzi umene ndinakupatsani inu ndi makolo
anu, ndidzaucotsa pamaso panga; 40ndipo ndidzakutengerani inu
citonzo camuyaya, ndi manyazi amuyaya, amene sadzaiwalika.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Za mitanga iwiri ya nkhuyu; za mtundu wao m'tsogolo

1Yehova anandionetsa ine, ndipo, taonani, mitanga iwiri ya nkhuyu
yoikidwa pakhomo pa Kacisi wa Yehova; Nebukadirezara mfumu ya
ku Babulo atacotsa am'nsinga Yekoniya mwana wace wa
Yehoyakimu, mfumu ya Yuda, ndi akuru a Yuda, ndi amisiri ndi
acipala, kuwacotsa ku Yerusalemu, nawatengera ku
Babulo. 2Mtanga umodzi unali ndi nkhuyu zabwinobwino, ngati
nkhuyu zoyamba kuca; ndipo mtanga umodzi unali ndi nkhuyu
zoipaipa, zosadyeka, zinali zoipa. 3Ndipo Yehova anati kwa ine,
Kodi uona ciani, Yeremiya? Ndipo ndinati, Nkhuyu, nkhuyu
zabwino, nzabwino ndithu; zoipazo nzoipa ndithu, zosadyeka poti
nzoipa. 4Ndipo mau a Yehova anadza kwa ine, kuti, 5Cifukwa
Yehova, Mulungu wa Israyeli, atero, Monga nkhuyu zabwino izi,
momwemo ndidzasamalira am'nsinga a Yuda, amene
ndawacotsera m'malo muno kunka ku dziko la Akasidi, kuwacitira
bwino. 6Pakuti ndidzaika maso anga pa iwo kuti ndiwacitire iwo
bwino, ndipo ndidzawabwezanso ku dziko ili: ndipo ndidzamangitsa
mudzi wao, osawapasula; ndi kuwabzyala, osawazula iwo. 7Ndipo
ndidzapatsa iwo mtima wakundidziwa, kuti ndine Yehova;
nadzakhala anthu anga, ndipo Ine ndidzakhala Mulungu wao;
pakuti adzabwera kwa Ine ndi mtima wao. 8Ndipo, monga nkhuyu
zoipa, zosadyeka, poti nzoipa; ntheradi atero Yehova, Comweco
ndidzapereka Zedekiya mfumu ya Yuda, ndi akulu ace, ndi otsala a
m'Yerusalemu, amene atsala m'dziko ili, ndi amene akhala m'dziko
la Aigupto. 9Ndipo ndidzawapatsa akhale coopsetsa coipa ku
maufumu a dziko lapansi; akhale citonzo ndi nkhani ndi coseketsa,
ndi citemberero, monse m'mene ndidzawapitikitsiramo. 10Ndipo
ndidzatuma lupanga, ndi njala, ndi caola mwa iwo, mpaka athedwa
m'dziko limene ndinapatsa iwo ndi makolo ao.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Atalangidwa Aisrayeli adzalangidwa amitundu ena omwe

1Mau amene anadza kwa Yeremiya za anthu onse a Yuda caka
cacinai ca Yehoyakimu mwana wace wa Yosiya, mfumu ya Yuda;
ndico caka coyamba ca Nebukadirezara mfumu ya ku
Babulo; 2amene Yeremiya ananena kwa anthu onse a Yuda, ndi
onse okhala m'Yerusalemu, kuti: 3Kuyambira caka cakhumi ndi
citatu ca Yosiya mwana wace wa Amoni, mfumu ya Yuda, kufikira
lero lomwe, zakazi makumi awiri ndi zitatu, mau a Yehova anafika
kwa ine, ndipo ndanena kwa inu, pouka mamawa ndi kunona;
koma simunamvera. 4Ndipo Yehova watuma kwa inu atumiki ace
onse ndiwo aneneri, pouka mamawa ndi kuwatuma; koma
simunamvera, simunachera khutu lanu kuti mumve; 5ndi kuti,
Mubwerere tsopano nonsenu, yense kuleka njira yace yoipa, ndi
zoipa za nchito zanu, ndi kukhala m'dziko limene Yehova anapatsa
inu ndi makolo anu, kuyambira kale kufikira muyaya; 6musatsate
milungu yina kuitumikira, ndi kuigwadira, musautse mkwiyo wanga
ndi nchito ya manja anu; ndingacitire inu coipa. 7Koma
simunandimvera Ine, ati Yehova; kuti muutse mkwiyo wanga ndi
nchito ya manja anu ndi kuonapo coipa inu. 8Cifukwa cace Yehova
wa makamu atero: Popeza simunamvera mau anga, 9taonani, Ine
ndidzatuma ndi kutenga mabanja onse a kumpoto, ati Yehova,
ndipo ndidzatuma kwa Nebukadirezara mfumu ya ku Babulo,
mtumiki wanga, ndipo ndidzatengera iwo pa dziko lino, ndi pa
okhalamo ace onse, ndi pa mitundu iyi yozungulira, ndipo
ndidzathetsa iwo ndithu, ndi kuwayesa iwo cizizwitso, ndi
cotsonyetsa, ndi bwinja lamuyaya. 10Ndiponso ndidzawacotsera
mau akusekera ndi mau akukondwera, ndi mau a mkwati, ndi mau
a mkwatibwi, mau a mphero, ndi kuwala kwa nyali. 11Ndipo dziko
lonseli lidzakhala labwinja, ndi cizizwitso, ndipo mitundu iyi
idzatumikira mfumu ya ku Babulo zaka makumi asanu ndi
awiri. 12Ndipo kudzakhala, zitapita zaka makumi asanu ndi awiri,
ndzidzalanga mfumu ya ku Babulo, ndi mtundu uja womwe, ati
Yehova, cifukwa ca mphulupulu zao, ndi dziko la Akasidi; ndipo
ndidzaliyesa mabwinja amuyaya. 13Ndipo ndidzatengera dzikolo
mau anga onse amene ndinanenera ilo, mau onse olembedwa
m'buku ili, amene Yeremiya wanenera mitundu yonse. 14Pakuti
mitundu yambiri ndi mafumu akuru adzayesa iwo atumiki ao;
ndipo ndidzabwezera iwo monga mwa macitidwe ao, monga mwa
nchito ya manja ao.
15Pakuti Yehova, Mulungu wa Israyeli, atero kwa ine, Tenga cikho
ca vinyo wa ukaliwu pa dzanja langa, ndi kumwetsa mitundu
yonse, imene ndikutumizirako. 16Ndipo adzamwa, nadzayenda
dzandi dzandi, nadzacita misala, cifukwa ca lupanga limene Ine

ndidzatumiza mwa iwo. 17Ndipo ndinatenga cikho pa dzanja la Yehova, ndinamwetsa mitundu yonse, imene Yehova ananditumizirako; 18Yerusalemu, ndi midzi ya Yuda, ndi mafumu ace omwe, ndi akuru ace, kuwayesa iwo bwinja, cizizwitso, cotsonyetsa, ndi citemberero; monga lero lino; 19Farao mfumu ya ku Aigupto, ndi atumiki ace, ndi akuru ace, ndi anthu ace onse; 20ndi anthu onse osanganizidwa, ndi mafumu onse a dziko la Uzi, ndi mafumu onse a dziko la Afilisti, ndi Asikeloni, ndi Gaza, ndi Ekroni, ndi otsala a Asdodi, 21Edomu, ndi Moabu, ndi ana a Amoni, 22ndi mafumu onse a Turo, ndi mafumu onse a Zidoni, ndi mafumu a cisumbu cimene ciri patsidya pa nyanja; 23Dedani, ndi Tema, ndi Buzi, ndi onse amene ameta m'mbali mwa tsitsi; 24ndi mafumu onse a Arabiya, ndi mafumu onse a anthu osanganizidwa okhala m'cipululu; 25ndi mafumu onse a Zimiri, ndi mafumu onse a Elamu, ndi mafumu onse a Medi, 26ndi mafumu onse a kumpoto, a kutari ndi a kufupi, wina ndi mnzace; ndi maufumu onse a dziko lapansi, okhala pansi pano; ndi mfumu ya Sesaki adzamwa pambuyo pao. 27Ndipo uziti kwa iwo, Atero Yehova wa makamu, Mulungu wa Israyeli: Imwani inu, ndi kuledzera, ndi kusanza, ndi kugwa, osanyamukanso konse, cifukwa ca lupanga limene ndidzatumiza mwa inu. 28Ndipo padzakhala, ngati akana kutenga cikho pa dzanja lako kuti amwe, uziti kwa iwo, Yehova wa makamu atero: Kumwa muzimwa. 29Pakuti, taonani, ndiyamba kucita coipa pa mudzi umene uchedwa ndi dzina langa, kodi inu mudzakhala osalangidwa konse? Simudzakhala osalangidwa; pakuti ndidzaitana lupanga ligwe pa onse okhala m'dziko lapansi, ati Yehova wa makamu. 30Cifukwa cace muwanenere iwo mau onse awa, ndi kuti kwa iwo, Yehova adzabangula kumwamba, nadzachula mau ace mokhalamo mwace moyera; adzabangulitsira khola lace; adzapfuula, monga iwo akuponda mphesa, adzapfuulira onse okhala m'dziko lapansi. 31Phokoso lidzadza ku malekezero a dziko lapansi; pakuti Yehova ali ndi mlandu ndi mitundu ya anthu, adzatsutsana ndi anthu onse; koma oipa, adzawapereka kulupanga, ati Yehova.
32Yehova wa makamu atero, Taonani, zoipa zidzaturuka ku mtundu kunka m'mitundu, ndipo namondwe adzauka kucokera ku malekezero a dziko lapansi. 33Ndipo akuphedwa a Yehova adzakhala tsiku lomwelo kucokera ku malekezero ena a dziko lapansi kunka ku malekezero ena a dzikolapansi, sadzaliridwa maliro, sadzasonkhanidwa, sadzaikidwa; adzakhala ngati ndowe panthaka. 34Kuwani, inu abusa, lirani, gubudukani, inu akuru a zoweta; pakuti masiku a kuphedwa kwanu akwanira ndithu, ndipo ndidzakuphwanyani inu, ndipo mudzagwa ngati cotengera cofunika. 35Ndipo abusa adzasowa pothawira, mkuru wa zoweta

adzasowa populumukira. 36Mau akupfuula abusa, ndi kukuwa
mkuru wa zoweta! pakuti Yehova asakaza busa lao. 37Ndipo makola
amtendere adzaonongeka cifukwa ca mkwiyo woopsa wa
Yehova. 38Wasiya ngaka yace, monga mkango; pakuti dziko lao
lasanduka cizizwitso cifukwa ca ukali wa lupanga losautsa, ndi
cifukwa ca mkwiyo wace waukali.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Yeremiya aneneratu za kupasuka kwa Kacisi ndi Yerusalemu. Atsutsidwapo afe

1Poyamba kukhala mfumu Yehoyakimu mwana wace wa Yosiya,
mfumu ya Yuda, panadza mau awa ocokera kwa Yehova,
kuti, 2Yehova atero: Ima m'bwalo la nyumba ya Yehova, ndi kunena
kwa midzi yonse ya Yuda, imene imadza kudzagwadira m'nyumba
ya Yehova, mau onse amene ndikuuza iwe kuti unene kwa iwo;
usasiyepo mau amodzi. 3Kapena adzamvera, nadzatembenuka,
yense kusiya njira yace yoipa; kuti ndileke coipa, cimene ndinati
ndiwacitire cifukwa ca kuipa kwa nchito zao. 4Ndipo iwe uziti kwa
iwo, Yehova atero: Ngati simudzandimvera Ine kuyenda m'cilamulo
canga, cimene ndaciika pamaso panu, 5kumvera mau a atumiki
anga aneneri, amene nditumа kwa inu, pouka mamawa ndi
kuwatuma iwo, koma simunamvera; 6pamenepo ndidzayesa
nyumba iyi ifanane ndi Silo, ndipo ndidzayesa mudzi uwu
citemberero ca kwa mitundu yonse ya dziko lapansi. 7Ndipo
ansembe ndi aneneri ndi anthu onse anamva Yeremiya alinkunena
mau awa m'nyumba ya Yehova. 8Ndipo panali, pamene Yeremiya
anatha kunena mau onse amene Yehova anamuuza iye kuti anene
kwa anthu onse, ansembe ndi aneneri ndi anthu onse anamgwira
iye, ndi kuti, Udzafa ndithu. 9Bwanji mwanenera m'dzina la Yehova,
kuti, Nyumba iyi idzafanana ndi Silo, mudzi uwu udzakhala bwinja
lopanda wokhalamo? Ndipo anthu onse anamsonkhanira Yeremiya
m'nyumba ya Yehova.
10Ndipo pamene akuru a Yuda anamva zimenezi, anakwera
kuturuka ku nyumba ya mfumu kunka ku nyumba ya Yehova; ndipo
anakhala pa khomo la cipata catsopano ca nyumba ya
Yehova. 11Ndipo ansembe ndi aneneri ananena kwa akuru ndi kwa
anthu onse, kuti, Munthu uyu ayenera kufa; pakuti wanenera
mudzi uwu monga mwamva ndi makutu anu. 12Pamenepo
Yeremiya ananena kwa akuru onse ndi kwa anthu onse, kuti,
Yehova ananditumа ine ndinenere nyumba iyi ndi mudzi uwu mau
onse amene mwamva. 13Cifukwa cace tsopano konzani njira zanu
ndi macitidwe anu, ndi kumvera mau a Yehova Mulungu wanu;
ndipo Yehova adzaleka coipa cimene ananenera inu. 14Koma ine,
taonani, ndiri m'manja anu; mundicitire ine monga mokomera ndi
moyenera m'maso anu. 15Koma mudziwe ndithu kuti, ngati
mudzandipha ine, mudzadzitengera nokha mwazi wosacimwa, ndi
pa mudzi uwu, ndi pa okhalamo ace; pakuti mwa ntheradi Yehova
wandituma kwa inu kuti ndinene mau onse awa m'makutu
anu. 16Pamenepo akuru ndi anthu onse anati kwa ansembe ndi
kwa aneneri, Munthu uyu sayenera kufa: pakuti watinenera ife
m'dzina la Yehova Mulungu wathu. 17Ndipo anauka akuru ena a

m'dziko, nati kwa msonkhano wa anthu, kuti, 18Mika Mmorasi
ananenera masiku a Hezekiya mfumu ya Yuda; ndipo iye ananena
kwa anthu onse a Yuda, kuti, Yehova wa makamu atero: Ziyoni
adzalimidwa ngati munda, Yerusalemu adzakhala miunda, ndi phiri
la nyumba longa misanje ya nkhalango. 19Kodi Hezekiya mfumu ya
Yuda ndi Yuda wonse anamupha iye konse? kodi sanamuopa
Yehova, napembedzera Yehova, ndipo Yehova analeka coipa
cimene ananenera iwo? Cotero tidzaicitira miyoyo yathu coipa
cacikuru. 20Ndipo panalinso munthu amene ananenera m'dzina la
Yehova, Uriya mwana wace wa Semaya wa ku Kiriati Yearimu;
ndipo iye ananenera mudzi uwu ndi dziko lino monga mwa mau
lonse a Yeremiya; 21ndipo pamene Yehoyakimu mfumu, ndi
amphamvu ace onse, ndi akuru onse, anamva mau ace, mfumu
inafuna kumupha iye; koma pamene Uriya anamva, anaopa,
nathawa, nanka ku Aigupto; 22ndipo Yehoyakimu mfumu anatuma
anthu ku Aigupto, Elinatanu mwana wace wa Akibori, ndi anthu
ena pamodzi ndi iye, anke ku Aigupto; 23ndipo anamturutsa Uriya
m'Aigupto, nanka naye kwa Yehoyakimu mfumu; amene
anamupha ndi lupanga, naponya mtembo wace m'manda a anthu
acabe. 24Koma dzanja la Ahikamu mwana wa Safani linali ndi
Yeremiya, kuti asampereke m'manja a anthu kuti amuphe.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Yeremiya awacenjeza agonje kwa mfumu ya ku Babulo

1Poyamba kukhala mfumu Yehoyakimu mwana wace wa Yosiya,
mfumu ya Yuda, mau awa anadza kwa Yeremiya kucokera kwa
Yehova, kuti, 2Yehova atero kwa ine: Udzipangire zomangira ndi
magori, nuziike pakhosi pako; 3nuzitumize kwa mfumu ya Edomu,
ndi kwa mfumu ya Moabu, ndi kwa mfumu ya ana a Amoni, ndi
kwa mfumu ya Turo, ndi kwa mfumu ya Zidoni, ndi dzanja la
amithenga amene afika ku Yerusalemu kwa Zedekiya mfumu ya
Yuda; 4nuwauze iwo anene kwa ambuyao, kuti, Yehova wa
makamu, Mulungu wa Israyeli atero: Muzitero kwa ambuyanu: 5Ine
ndinalenga dziko lapansi, anthu ndi nyama zokhala m'dzikomo, ndi
mphamvu yanga yaikuru ndi mkono wanga wotambasuka; ndipo
ndinapereka ilo kwa iye amene ayenera pamaso panga. 6Tsopano
ndapereka maiko onse awa m'manja a Nebukadinezara mfumu ya
ku Babulo, mtumiki wanga; ndiponso nyama za kuthengo
ndampatsa iye kuti zimtumikire. 7Ndipo amitundu, onse
adzamtumikira iye, ndi mwana wace, ndi mdzukulu wace, mpaka
yafika nthawi ya dziko lace; ndipo amitundu ambiri ndi mafumu
akuru adzamuyesa iye mtumiki wao. 8Ndipo padzakhala, kuti
mtundu ndi ufumu umene sudzamtumikira Nebukadinezara
yemweyo mfumu ya ku Babulo, mtundu umenewo Ine ndidzalanga,
ati Yehova, ndi lupanga, ndi njala, ndi caola, mpaka nditatha onse
ndi dzanja lace. 9Koma inu, musamvere aneneri anu, kapena
akuombeza anu, kapena maloto anu, kapena alauli anu, kapena
obwebweta anu, Musadzatumikira mfumu ya ku Babulo; 10kakuti
iwo akunenerani inu zonama, kuti akucotseni inu m'dziko lanu,
kunka kutari kuti ndikupitikitseni inu, ndipo inu
mudzathedwa. 11Koma mtundu umene udzaika khosi lao pansi pa
gori la mfumu ya ku Babulo, ndi kumtumikira iye, mtundu umene
ndidzaulola ukhalebe m'dziko lao, ati Yehova; ndipo adzalilima,
nadzakhala momwemo.
12Ndipo ndinanena kwa Zedekiya mfumu ya Yuda monga mau onse
amenewa, kuti, Longani makosi anu m'gori la mfumu ya ku Babulo,
ndi kumtumikira iye ndi anthu ace, ndipo mudzakhala ndi
moyo. 13Mudzaferanji, iwe ndi anthu anu, ndi lupanga ndi njala, ndi
caola, monga wanena Yehova za mtundu umene ukana
kumtumikira mfumu ya ku Babulo? 14Musamvere mau a aneneri
amene anena ndi inu, kuti, simudzamtumikira mfumu ya ku
Babulo; pakuti akunenerani zonama. 15Pakuti sindinawatuma iwo,
ati Yehova, koma anenera zonama m'dzina langa; kuti
ndikupitikitseni inu, kuti mudzathedwe, inu, ndi aneneri amene
anenera kwa inu. 16Ndiponso ndinanena kwa ansembe ndi kwa
anthu onsewa, kuti, Yehova atero: Musamvere mau a aneneri anu

amene akunenerani inu, kuti, Taonani, zipangizo za nyumba ya Yehova zidzatengedwanso ku Babulo posacedwa; pakuti akunenerani inu zonama. 17Musamvere amenewa; mtumikireni mfumu ya ku Babulo, ndipo mudzakhala ndi moyo; cifukwa canji mudzi uwu udzakhala bwinja? 18Koma ngati ndiwo aneneri, ndipo ngati mau a Yehova ali ndi iwo, tsopano apembedzere Yehova wa makamu, kuti zipangizo zotsala m'nyumba ya Yehova, ndi m'nyumba ya mfumu ya Yuda, ndi ku Yerusalemu, zisanke ku Babulo. 19Pakuti Yehova wa makamu atero, za zoimiritsa, ndi za thawale, ndi za zoikirapo, ndi za zipangizo zotsala m'mudzi uwu, 20zimene sanazitenga Nebukadinezara mfumu ya ku Babulo, pamene anamtenga ndende Yekoniya mwana wace wa Yehoyakimu, mfumu ya Yuda, kucokera ku Yerusalemu kunka ku Babulo; ndi akuru onse a Yuda ndi Yerusalemu; 21inde, atero Yehova, Mulungu wa Israyeli, za zipangizo zotsala m'nyumba ya Yehova, ndi m'nyumba ya mfumu ya Yuda, ndi ku Yerusalemu; 22adzanka nazo ku Babulo, kumeneko zidzakhala, mpaka tsiku limene ndidzayang'anira iwo, ati Yehova; pamenepo ndidzazikweza, ndi kuzibwezera kumalokuno.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Yeremiya atsutsana ndi mneneri wonyenga, Hananiya

1Ndipo panali caka comweco, poyamba Zedekiya kukhala mfumu
ya Yuda, caka cacinai, mwezi wacisanu, kuti Hananiya mwana wa
Azuri mneneri, amene anali wa ku Gibeoni, ananena ndi ine
m'nyumba ya Yehova, pamaso pa ansembe ndi pa anthu onse,
kuti, 2Atero Yehova wa makamu, Mulungu wa Israyeli, kuti,
Ndatyola gori la mfumu ya ku Babulo. 3Zisanapite zaka ziwiri
zamphumphu Ine ndidzabwezeranso kumalo kuno zipangizo zonse
za m'nyumba ya Yehova, zimene Nebukadinezara mfumu ya ku
Babulo anazicotsa muno, kunka nazo ku Babulo; 4ndipo
ndidzabwezeranso kumalo kuno Yekoniya mwana wace wa
Yehoyakimu, mfumu ya Yuda, ndi am'nsinga onse a Yuda, amene
ananka ku Babulo, ati Yehova: pakuti ndidzatyola gori la mfumu ya
ku Babulo. 5Ndipo Yeremiya mneneri anati kwa Hananiya mneneri
pamaso pa ansembe, ndi pamaso pa anthu onse amene anaima
m'nyumba ya Yehova, 6Yeremiya mneneri anati, Amen: Yehova
acite cotero: Yehova atsimikize mau ako amene wanenera,
abwezerenso zipangizo za nyumba ya Yehova, ndi onse amene
anacotsedwa am'nsinga, kucokera ku Babulo kudza kumalo
kuno. 7Koma mumvetu mau awa amene ndinena m'makutu anu,
ndi m'makutu a anthu onse: 8Aneneri amene analipo kale
ndisanakhale ine, nimusanakhale inu, ananenera maiko ambiri, ndi
maufumu akuru, za nkhondo, ndi za coipa, ndi za caola. 9Mneneri
amene anenera za mtendere, pamene mau a mneneri adzacitidwa,
pamenepo mneneri adzadziwika, kuti Yehova anamtuma
ndithu. 10Pamenepo Hananiya anacotsa gori pa khosi la Yeremiya,
nalityola. 11Ndipo Hananiya ananena pamaso pa anthu onse, kuti,
Yehova atero: Comweco ndidzatyola gori la Nebukadinezara
mfumu ya Babulo zisanapite zaka ziwiri zamphumphu kulicotsa pa
khosi la amitundu onse. Ndipo Yeremiya mneneri anacoka. 12Ndipo
mau a Yehova anadza kwa Yeremiya, atatyola Hananiya mneneri
gori kulicotsa pa khosi la Yeremiya, kuti, 13Pita, nunene kwa
Hananiya, kuti Yehova atero: Watyola magori amtengo; koma
udzapanga m'malo mwao magori acitsulo. 14Pakuti atero Yehova
wa makamu, Mulungu wa Israyeli: Ndaika gori lacitsulo pa khosi la
amitundu onsewa, kuti amtumikire Nebukadinezara mfumu ya ku
Babulo; ndipo adzamtumikira iye; ndipo ndampatsanso nyama za
kuthengo. 15Ndipo Yeremiya mneneri ananena kwa Hananiya
mneneri, Tamvatu, Hananiya; Yehova sanakutuma iwe; koma
ukhulupiritsa anthu awa zonama. 16Cifukwa cace Yehova atero,
Taona, Ine ndidzakucotsa iwe kudziko; caka cino udzafa, pakuti
wanena zopikisana ndi Yehova. 17Ndipo anafa Hananiya caka
comweco mwezi wacisanu ndi ciwiri.

Kalata wa Yeremiya wolembera kwa Ayuda otengedwa kunka ku Babulo

1Amenewa ndi mau a kalata uja anatumiza Yeremiya mneneri
kucokera ku Yerusalemu kunka kwa akuru otsala a m'nsinga, ndi
kwa ansembe, ndi kwa aneneri, ndi kwa anthu onse, amene
Nebukadnezara anawatenga ndende ku Yerusalemu kunka ku
Babulo; 2anatero atacoka ku Yerusalemu Yekoniya mfumu ndi
amace a mfumu ndi adindo ndi akuru a Yuda ndi a ku Yerusalemu,
ndi amisiri, ndi acipala, 3anatumiza kalatayo m'dzanja la Elasa
mwana wace wa Safani, ndi Gemariya mwana wace wa Hilikiya,
amene Zedekiya mfumu ya Yuda anawatuma ku Babulo kwa
Nebukadinezara mfumu ya ku Babulo, kuti, 4Yehova wa makamu,
Mulungu wa Israyeli atero, kwa am'nsinga onse, amene
ndinawatenga ndende ku Yerusalemu kunka nao ku
Babulo: 5Mangani nyumba, khalani m'menemo; limani minda,
idyani zipatso zace; 6tengani akazi, balani ana amuna ndi akazi;
kwatitsani ana anu amuna, patsani ananu akazi kwa amuna, kuti
abale ana amuna ndi akazi; kuti mubalane pamenepo,
musacepe. 7Nimufune mtendere wa mudzi umene
ndinakutengerani am'nsinga, nimuwapempherere kwa Yehova;
pakuti mwa mtendere wace inunso mudzakhala ndi
mtendere. 8Pakuti Yehova wa makamu, Mulungu wa Israyeli atero:
Aneneri anu ndi akuombeza anu amene akhala pakati panu,
asakunyengeni inu, musamvere maloto anu amene
mulotetsa. 9Pakuti anenera kwa inu zonama m'dzina langa;
sindinatuma iwo, ati Yehova. 10Pakuti Yehova atero, kuti, Zitapita
zaka makumi asanu ndi awiri pa Babulo, ndidzakuyang'anirani inu,
ndipo ndidzakucitirani inu mau anga abwino, ndi kubwezera inu
kumalo kuno. 11Pakuti ndidziwa malingiriro amene ndilingiririra inu,
ati Yehova, malingiriro a mtendere, si a coipa, akukupatsani inu
adzukulu ndi ciyembekezero. 12Pamenepo mudzandiitana Ine,
ndipo mudzanka ndi kupemphera kwa Ine, ndipo ndidzakumverani
inu. 13Ndipo mudzandifuna Ine, ndi kundipeza, pamene mundifuna
ndi mtima wanu wonse. 14Ndipo ndidzapezedwa ndi inu, ati
Yehova, ndidzabwezanso undende wanu, ndipo ndidzasonkhanitsa
inu kwa mitundu yonse, ndi kumalo konse kumene
ndinakupitikitsirani inu, ati Yehova; ndipo ndidzakubwezeraninso
kumalo kumene ndinakutengani inu andende. 15Pakuti mwati,
Yehova watiutsira ife aneneri m'Babulo. 16Pakuti Yehova atero za
mfumu imene ikhala pa mpando wacifumu wa Davide, ndi za
anthu onse amene akhala m'mudzi uno, abale anu amene
sanaturukira pamodzi ndiinu kundende; 17Yehova wa makamu
atero: Taonani, ndidzatuma pa iwo lupanga, ndi njala, ndi caola,

ndipo ndidzayesa iwo onga nkhuyu zoola, zosadyeka, pokhala nzoipa. 18Ndipo ndidzatsata iwe ndi lupanga, ndi njala, ndi caola, ndipo ndidzawapereka akhale oopsyetsa m'maufumu onse a dziko la pansi, akhale citemberero, ndi codabwitsa, ndi cotsonyetsa, ndi citonzo, kwa mitundu yonse kumene ndinawapitikitsirako; 19cifukwa sanamvera mau anga, ati Yehova, amene ndinawatumizira ndi atumiki anga aneneri, ndi kuuka mamawa ndi kuwatuma, koma munakana kumva, ati Yehova. 20Pamenepo tamvani inu mau a Yehova, inu nonse a m'ndende, amene ndacotsa m'Yerusalemu kunka ku Babulo. 21Atero Yehova wa makamu, Mulungu wa Israyeli, za Ahabu mwana wace wa Koliya, ndi za Zedekiya mwana wace wa Maseya, amene anenera zonama m'dzina langa: Taonani, Ndidzawapereka m'dzanja la Nebukadirezara mfumu ya ku Babulo; ndipo Iye adzawapha pamaso panu; 22ndipo am'nsinga onse a Yuda amene ali m'Babulo adzatemberera pali iwo, kuti, Yehova akucitire iwe monga Zedekiya ndi Ahabu, amene mfumu ya ku Babulo inaoca m'moto; 23cifukwa anacita zopusa m'Israyeli, nacita cigololo ndi akazi a anansi ao, nanena mau onama m'dzina langa, amene ndinawauza kuti asanene; Ine ndine wodziwa, ndi mboni, ati Yehova.
24Ndipo za Semaya Mnehelamu uzinena, kuti, 25Atero Yehova wa makamu, Mulungu wa Israyeli, kuti, Cifukwa watumiza akalata m'dzina lako iwe mwini kwa anthu onse amene akhala ku Yerusalemu, ndi kwa Zefaniya mwana wace wa Maseya wansembe, ndi kwa ansembe onse, kuti. 26Yehova anakuyesa iwe wansembe m'malo mwa Yehoyada wansembe, kuti iwe ndi anzako mudzakhale akapitao m'nyumba ya Yehova, oyang'anira munthu yense wamisala, wodziyesa mneneri, kuti umuike iye m'zigologolo ndi m'gori. 27Ndipo tsopano, walekeranji kumdzudzula Yeremiya wa ku Anatoti, amene amadziyesa mneneri wanu, 28popeza watitumizira mau ku Babulo, akuti, Undende udzakhalitsa; mangani nyumba, khalani m'menemo; limani minda, idyani zipatso zao? 29Ndipo Zefaniya wansembe anawerenga kalata amene m'makutu a Yeremiya mneneri. 30Ndipo anadza mau a Yehova kwa Yeremiya, akuti, 31Uwatumizire mau am'nsinga onse, akuti, Atero Yehova za Semaya Mnehelamu: Cifukwa Semaya wanenera kwa inu, koma Ine sindinamtuma, ndipo anakukhulupiritsani zonama; 32cifukwa cace atero Yehova, Taonani, ndidzalanga Semaya Mnehelamu, ndi mbeu zace; sadzakhala ndi munthu wakukhala mwa anthu awa, sadzaona za bwino ndidzacitira anthu anga, ati Yehova: cifukwa wanena zopikisana ndi Yehova.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Yehova alonjeza kubweza undende wa anthu a Israyeli

1Mau amene anadza kwa Yeremiya kucokera kwa Yehova,
kuti, 2Atero Yehova, Mulungu wa Israyeli, kuti, Lemba m'buku mau
onse amene ndanena kwa iwe. 3Pakuti, taona, masiku adzadza, ati
Yehova, amene ndidzabwezanso undende wa anthu anga Aisrayeli
ndi Ayuda, ati Yehova; ndipo ndidzawabwezera ku dziko limene
ndinapatsa makolo ao. Ndipo adzakhala nalo.
4Awa ndi mau ananena Yehova za Israyeli ndi Yuda. 5Pakuti Yehova
atero: Tamva ife mau akunthunthumira, ndi amantha, si
amtendere. 6Funsani tsopano, ndi kuona ngati mwamuna aona
mwana; cifukwa canji ndiona mwamuna ndi manja ace pa cuuno
cace, monga mkazi alinkubala, ndi nkhope zao
zotumbuluka? 7Kalanga ine! pakuti nlalikuru tsikulo, palibe lina
lotere; ndi nthawi ya msauko wa Yakobo; koma adzapulumuka
m'menemo. 8Pakuti padzakhala tsiku lomwelo, ati Yehova wa
makamu, kuti ndidzatyola gori lace pakhosi pako, ndipo ndidzadula
zomangira zako; ndipo alendo sadzamuyesanso iye mtumiki
wao; 9koma adzamtumikira Yehova Mulungu wao, ndi Davide
mfumu yao, imene ndidzawaukitsira. 10Ndipo usaope, iwe Yakobo
mtumiki wanga, ati Yehova; usaope, iwe Israyeli; pakuti, taona,
ndidzakupulumutsa iwe kutari, ndi mbeu zako ku dziko la undende
wao; ndipo Yakobo adzabwera, nadzakhala ndi mtendere, ndipo
adzakhala cete, palibe amene adzamuopsya. 11Pakuti Ine ndiri ndi
iwe, ati Yehova, kuti ndipulumutse iwe; koma ndidzatha ndithu
amitundu onse amene ndinakumwazira mwa iwo, koma
sindidzatha iwe ndithu; koma ndidzakulangiza iwe ndi ciweruziro,
ndipo sindidzakuyesa wosaparamula.
12Pakuti atero Yehova, Kulaswa kwako kuti kosapoleka ndi bala lako
liri lowawa. 13Palibe amene adzanenera mlandu wako, ulibe
mankhwala akumanga nao bala lako. 14Mabwenzi ako onse
anakuiwala iwe; salikukufuna iwe; pakuti ndakulasa ndi bala la
mdani, ndi kulanga kwa wankhanza; cifukwa ca mphulupulu yako
yaikuru, cifukwa zocimwa zako zinacuruka. 15Cifukwa canji ulilira
bala lako? kuphwetekwa kwako kuli kosapoleka; cifukwa ca
mphulupulu yako yaikuru, cifukwa zocimwa zako zinacuruka,
ndakucitira iwe izi. 16Cifukwa cace iwo akulusira iwe
adzalusidwanso; ndi adani ako onse, adzanka kuundende onsewo;
ndipo iwo adzakufunkha iwe adzakhala cofunkha, ndipo onse
akulanda iwe ndidzapereka kuti zilandidwe zao. 17Pakuti
ndidzakubwezera iwe moyo, ndipo ndidzapoletsa mabala ako, ati
Yehova; cifukwa anacha iwe wopitikitsidwa, nati, Ndiye Ziyoni,
amene kulibe munthu amfuna. 18Atero Yehova: Taonani,
ndidzabwezanso undende wa mahema a Yakobo, ndipo ndidzacitira

cifundo zokhalamo zace, ndipo mudzi udzamangidwa pamuunda pace, ndi cinyumba cidzakhala momwe. 19Ndipo padzaturuka pa izo mayamikiro ndi mau a iwo okondwerera; ndipo ndidzacurukitsa iwo, sadzakhala owerengeka; ndidzawacitiranso ulemu, sadzacepa. 20Ana aonso adzakhala monga kale, ndipo msonkhano wao udzakhazikika pamaso panga, ndipo ndidzalanga onse amene akupsinja iwo. 21Ndipo mkuru wao adzakhala mwa iwo, ndi wolamulira wao adzaturuka pakati pao; ndipo ndidzamyandikitsa iye, ndipo adzayandikira kwa Ine, pakuti iye wolimba mtima kuyandikira kwa Ine ndani? ati Yehova. 22Ndipo inu mudzakhala anthu anga, ndipo ndidzakhala Mulungu wanu.
23Taonani, cimphepo ca Yehova, kupsya mtima kwace, caturuka, cimphepo cakukokolola: cidzagwa pamtu pa oipa. 24Mkwiyo waukali wa Yehova sudzabwerera, mpaka wacita, mpaka watha zomwe afuna kucita m'mtima mwace: masiku akumariza mudzacizindikira.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Mwa cikondi ca Mulungu adzabweza Israyeli

1Nthawi yomweyo, ati Yehova, ndidzakhala Mulungu wa mabanja
onse a Israyeli, ndipo iwo adzakhala anthu anga. 2Atero Yehova,
Anthu opulumuka m'lupanga anapeza cisomo m'cipululu; Israyeli,
muja anakapuma. 3Yehova anaonekera kwa ine kale, ndi kuti, Inde,
ndakukonda iwe ndi cikondi cosatha; cifukwa cace ndakukoka iwe
ndi kukukomera mtima. 4Ndidzamangitsanso mudzi wako, ndipo
udzamangidwa, iwe namwali wa Israyeli; udzakometsedwanso ndi
mangaka, ndipo udzaturukira masewero a iwo
akukondwerera. 5Ndiponso udzalima minda ya mphesa pa mapiri a
Samariya; akunka adzanka, nadzayesa zipatso zace
zosapatulidwa. 6Pakuti lidzafika tsiku, limene alonda a pa mapiri a
Efraimu adzapfuula, Ukani inu, tikwere ku Ziyoni kwa Yehova
Mulungu wathu. 7Pakuti Yehova atero, Yimbirirani Yakobo ndi
kukondwa, pfuulirani mtundu woposawo; lalikirani, yamikirani, ndi
kuti, Yehova, mupulumutse anthu anu, ndi otsala a
Israyeli, 8Taonani, ndidzatenga iwo ku dziko la kumpoto,
ndidzasonkhanitsa iwo ku malekezero a dziko lapansi, pamodzi ndi
osaona ndi opunduka mwendo, mkazi amene ali ndi pakati ndi
mkazi alinkubala pamodzi; khamu lalikuru lidzabwera
kuno. 9Adzadza ndi kulira, ndipo ndidzawatsogolera ndi
mapembedzero, ndidzawayendetsa ku mitsinje yamadzi, m'njira
yoongoka m'mene sadzapunthwa, pakuti ndiri Atate wace wa
Israyeli, ndipo Efraimu ali mwana wanga woyamba.
10Tamvani mau a Yehova, amitundu inu, lalikirani m'zisumbu
zakutari; ndi kuti, Iye amene anabalalitsa Israyeli adzasonkhanitsa,
nadzamsunga, monga mbusa acita ndi zoweta zace. 11Pakuti
Yehova wapulumutsa Yakobo, namuombola iye m'dzanja la iye
amene anamposa mphamvu, 12Ndipo adzadza nadzayimba pa
msanje wa Ziyoni, nadzasonkhanira, ku zokoma za Yehova,
kutirigu, ndi kuvinyo, ndi mafuta, ndi kwa ana a zoweta zazing'ono
ndi zazikuru; ndipo moyo wao udzakhala ngati munda wamicera;
ndipo, sadzakhalanso konse ndi cisoni. 13Ndipo namwali
adzasangalala m'masewero, ndi anyamata ndi nkhalamba
pamodzi; pakuti ndidzasandutsa kulira kwao kukhale kukondwera,
ndipo ndidzatonthoza mitima yao, ndi kuwasangalatsa iwo asiye
cisoni cao. 14Ndipo ndikhutitsa moyo wa ansembe ndi mafuta,
ndipo anthu anga adzakhuta ndi zokoma zanga, ati Yehova.

Rakeli adzatonthozedwa

15Atero Yehova: Mau amveka m'Rama, maliro ndi kulira
kwakuwawa, Rakeli alinkulirira ana ace; akana kutonthozedwa
mtima pa ana ace, cifukwa palibe iwo. 16Yehova atero: Letsa mau
ako asalire, ndi maso anu asagwe misozi; pakuti nchito yako

idzalandira mphoto, ati Yehova; ndipo adzabweranso kucokera ku
dziko la mdani. 17Ndipo ciripo ciyembekezero ca citsirizo cako, ati
Yehova; ndipo ana ako adzafikanso ku malire ao. 18Kumva ndamva
Efraimu alinkulirira kotero, Mwandilanga ine, ndipo ndalangidwa,
monga mwana wa ng'ombe wosazolowera gori; munditembenuze
ine, ndipo ine ndidzatembenuka; pakuti inu ndinu Yehova Mulungu
wanga. 19Pakuti nditatembenuka, ndinalapa; nditalangizidwa,
ndinamenya pa ncafu yanga; ndinakhala ndi manyazi, inde,
ndinapepulidwa, cifukwa ndinasenza citonzo ca ubwana
wanga. 20Kodi Efraimu ndiye mwana wanga wokondedwa? Kodi
ndiye mwana wokondweretsa? nthawi zonse zoti ndimnenera
zomtsutsa, pakuti ndimkumbukiranso ndithu; cifukwa cace
mumtima mwanga ndimlirira; ndidzamcitiradi cifundo, ati Yehova.

Aisrayeli adzakhalanso bwino m'dziko mwao

21Taimitsa zizindikiro, udzipangire zosonyeza; taika mtima wako
kuyang'anira mseu wounda, njira imene unapitamo;
tatembenukanso, iwe namwali wa Israyeli, tatembenukiranso ku
midzi yako iyi. 22Udzayenda kwina ndi kwina masiku angati; iwe
mwana wamkazi wobwerera m'mbuyo? pakuti Yehova walenga
catsopano m'dziko lapansi: mkazi adzasanduka mphongo.
23Atero Yehova wa makamu, Mulungu wa Israyeli, Kawirinso
adzanena mau awa m'dziko la Yuda ndi m'midzi yace, pamene
ndibwezanso undende wao; Yehova akudalitse iwe, wokhalamo
cilungamo, iwe phiri lopatulika. 24Ndipo Yuda ndi midzi yace yonse
adzakhalamo pamodzi; alimi, ndi okusa zoweta. 25Pakuti
ndakhutidwa mtima wolema, ndadzazanso mtima uli wonse
wacisoni. 26Pamenepo ndinauka, ndinaona; ndipo tulo tanga
tinandizunira ine. 27Taonani, masiku adza, ati Yehova, amene
ndidzafesera nyumba ya Israyeli ndi nyumba ya Yuda ndi mbeu ya
anthu ndi mbeu ya nyama. 28Ndipo padzakhala kuti, monga
ndayang'anira iwo kuzula ndi kupasula ndi kugwetsa, ndi kuononga
ndi kusautsa; momwemo ndidzayang'anira iwo kumangitsa mudzi
ndi kubzyala, ati Yehova. 29Masiku omwewo sadzanenanso, Atate
adya mphesa zowawa, ndi mano a ana ayayamira. 30Koma yense
adzafa cifukwa ca mphulupulu yace; yense amene adya mphesa
zowawa, mano ace adzayayamira.

Pangano latsopano pakati pa Mulungu ndi anthu ace

31Taonani, masiku adza, ati Yehova, ndipo ndidzapangana pangano
latsopano ndi nyumba ya lsrayeli, ndi nyumba ya Yuda; 32si monga
pangano limene ndinapangana ndi makolo ao tsiku lija
ndinawagwira manja kuwaturutsa m'dziko la Aigupto; pangano
langa limenelo analiswa, ngakhale ndinali mbuyao, ati
Yehova. 33Koma ili ndi pangano limene ndidzapangana ndi nyumba
ya Israyeli atapita masiku aja, ati Yehova; ndidzaika cilamulo canga

m'kati mwao, ndipo m'mtima mwao ndidzacilemba; ndipo
ndidzakhala Mulungu wao, nadzakhala iwo anthu anga; 34ndipo
sadzaphunzitsa yense mnansi wace, ndi yense mbale wace, kuti,
Mudziwe Yehova; pakuti iwo onse adzandidziwa, kuyambira
wamng'ono kufikira wamkuru wa iwo, ati Yehova; pakuti
ndidzakhululukira mphulupulu yao, ndipo sindidzakumbukira cimo
lao. 35Yehova atero, amene apatsa dzuwa kuti liunikire usana, ndi
malemba a mwezi ndi a nyenyezi kuti aunikire usiku, amene
atonthoza nyanja, pamene mafunde ace agabvira; Yehova wa
makamu ndi dzina lace: 36Ngati malembawa acoka pamaso panga,
ati Yehova, pamenepo mbeunso ya Israyeli idzaleka kukhala
mtundu pamaso panga ku nthawi zonse. 37Atero Yehova, Ngati
ukhoza kuyesa thambo la kumwamba, ndi kusanthula pansi maziko
a dziko, pamenepo ndidzacotsa mbeu zonse za Israyeli cifukwa ca
zonse anazicita, ati Yehova. 38Taonani, masiku adza, ati Yehova,
amene mudziwu udzamangidwira Yehova kuyambira pa nsanja ya
Hananeli kufikira ku cipata ca kungondya. 39Ndipo cingwe coyesera
cidzaturukanso kulunjika ku citunda ca Garebi, ndipo
cidzazungulira kunka ku Goa. 40Ndipo cigwa conse ca mitembo, ndi
ca phulusa, ndi minda yonse: kufikira ku mtsinje wa Kidroni,
kufikira kungondya kwa cipata ca akavalo kuloza kum'mawa,
ponsepo padzapatulikira Yehova; sipadzazulidwa,
sipadzagwetsedwa konse ku nthawi zamuyaya.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Yeremiya atsekeredwa m'kaidi nagula munda wa Hanameli

1Mau amene anadza kwa Yeremiya kucokera kwa Yehova caka
cakhumi ca Zedekiya mfumu ya Yuda, cimene cinali caka cakhumi
ndi cisanu ndi citatu ca Nebukadirezara. 2Nthawi yomweyo
nkhondo ya mfumu ya Babulo inamangira Yerusalemu misasa;
ndipo Yeremiya mneneri anatsekeredwa m'bwalo la kaidi, linali ku
nyumba ya mfumu ya Yuda. 3Pakuti Zedekiya mfumu ya Yuda
inamtsekera iye, nati, Cifukwa canji ulinkunenera, kuti, Yehova
atero, Taonani, ndidzapereka mudzi uwu m'dzanja la mfumu ya
Babulo, ndipo iye adzaulanda, 4ndipo Zedekiya mfumu ya Yuda
sadzapulumuka m'dzanja la Akasidi, koma adzaperekedwadi
m'dzanja la mfumu ya Babulo, ndipo adzanena ndi iye pakamwa
ndi pakamwa, ndipo adzaonana maso ndi maso; 5ndipo
adzatsogolera Zedekiya kunka ku Babulo, ndipo adzakhala komwe
kufikira ndidzamzonda, ati Yehova: ngakhale mudzamenyana ndi
Akasidi, simudzapindula konse?
6Ndipo Yeremiya anati, Mau a Yehova anadza kwa ine,
kuti, 7Taonani, Hanameli mwana wa Salumu mbale wa atate wako
adzadza kwa iwe, kuti, Ugule munda wanga uli ku Anatoti; pakuti
mphamvu yakuombola ndi yako kuugula. 8Ndipo Hanameli mwana
wa mbale wa atate wanga anadza kwa ine m'bwalo la kaidi monga
mwa mau a Yehova, nati kwa ine, Gulatu munda wanga, wa ku
Anatoti, m'dziko la Benjamini; pakuti mphamvu yakulowa ndi
yakuombola ndi yako; udzigulire wekha. Pamenepo ndinadziwa kuti
awa ndi mau a Yehova. 9Ndipo ndinagula mundawo wa ku Anatoti
kwa Hanameli mwana wa cibale wa atate wanga, ndimyesera
ndalama, masekele khumi ndi asanu ndi awiri a siliva. 10Ndipo
ndinalemba cikalataco, ndicisindikiza, ndiitana mboni zambiri,
ndiyesa ndalama m'miyeso. 11Ndipo ndinatenga kalata wogulira,
wina wosindikizidwa, monga mwa lamulo ndi mwambo, ndi wina
wobvundukuka; 12ndipo ndinapereka kalata wogulirayo kwa Baruki
mwana wa Neriya, mwana wa Maseya, pamaso pa Hanameli
mwana wa mbale wa atate wanga, ndi pamaso pa mboni zimene
zinalemba pa kalata wogulirayo, pamaso pa Ayuda onse okhala
m'bwalo la kaidi. 13Ndipo ndinauza Baruki pamaso pao,
kuti, 14Yehova wa makamu, Mulungu wa Israyeli atero; Tenga
akalata awa, kalata uyu wogulira, wosindikizidwa, ndi kalata uyu
wobvundukuka, nuwaike m'mbiya yadothi; kuti akhale masiku
ambiri. 15Pakuti Yehova wa makamu, Mulungu wa Israyeli atero:
Nyumba ndi minda ndi minda yamphesa idzagulidwanso m'dziko
muno.

Pemphero la Yeremiya

16Ndipo nditapereka kalata wogulirayo kwa Baruki mwana wa
Neriya, ndinapemphera kwa Yehova, kuti, 17Ha! Yehova Mulungu,
taonani, Inu munalenga kumwamba ndi dziko lapansi ndi
mphamvu yanu yaikuru ndi mkono wanu wotambasuka; palibe
cokulakani Inu; 18a amene mucitira cifundo anthu zikwi;
nimubwezera mphulupulu ya atate m'cifuwa ca ana ao a pambuyo
pao, dzina lace ndi Mulungu wamkuru, wamphamvu, Yehova wa
makamu; 19wamkuru, m'upo, wamphamvu m'nchito; maso anu ali
otsegukira njira zonse za ana a anthu; kuti mupatse yense monga
mwa cipatso ca macitidwe ace; 20amene munaika zizindikiro ndi
zodabwitsa m'dziko la Aigupto, mpaka lero lomwe, m'Israyeli ndi
mwa anthu ena; nimunadzitengera mbiri, monga lero
lomwe; 21ndipo munaturutsa anthu anu Israyeli m'dziko la Aigupto
ndi zizindikiro, ndi zodabwitsa, ndi dzanja lamphamvu, ndi mkono
wotambasuka, ndi mantha ambiri; 22ndipo munawapatsa iwo dziko
ili, limene munalumbirira makolo ao kuti mudzawapatsa, dziko
moyenda mkaka ndi uci; 23ndipo analowa, nakhalamo; koma sa
namvera mau anu, sanayenda m'cilamulo canu; sanacita kanthu
ka zonse zimene munawauza acite; cifukwa cace mwafikitsa pa
iwo coipa conseci; 24taonani mitumbira, yafika kumudzi kuugwira,
ndipo mudzi uperekedwa m'dzanja la, Akasidi olimbana nao,
cifukwa ca lupanga, ndi cifukwa ca njala, ndi cifukwa ca caola;
ndipo cimene munacinena caoneka; ndipo, taonani,
muciona. 25Ndipo Inu Yehova Mulungu mwati kwa ine, Udzigulire
munda ndi ndalama, nuitane mboni; koma mudzi waperekedwa
m'manja a Akasidi.

Mulungu anenetsa kuti Aisrayeli adzalangidwa, nalonjeza kuwalanditsanso

26Ndipo anadza mau a Yehova kwa Yeremiya, kuti, 27Taona, Ine
ndine Yehova, Mulungu wa anthu lonse; kodi kuli kanthu kondilaka
Ine?
28Cifukwa cace Yehova atero: Taona, ndidzapereka mudziwu
m'dzanja la Akasidi, m'dzanja la Nebukadirezara mfumu ya ku
Babulo, ndipo iye adzaulanda, 29ndipo Akasidi, olimbana ndi mudzi
uwu, adzafika nadzayatsa mudziwu, nadzautentha, pamodzi ndi
nyumba, zimene anafukizira Baala, pa macitidwe ao, ndi
kutsanulirira milungu yina nsembe zothira, kuti autse mkwiyo
wanga. 30Pakuti ana a Israyeli ndi ana a Yuda anacita zoipa zokha
zokha pamaso panga ciyambire ubwana wao, pakuti ana a Israyeli
anandiputa Ine kokha kokha ndi nchito ya manja ao, ati
Yehova. 31Pakuti mudzi uwu unali woutsa mkwiyo wanga ndi ukali
wanga kuyambira tsiku lija anaumanga mpaka lero, kuti ndiucotse
pamaso panga; 32cifukwa ca zoipa zonse za ana a Israyeli ndi za
ana a Yuda, zimene anandiputa nazo Ine, iwowo, mafumu ao, akulu

ao, ansembe ao, aneneri ao, ndi anthu a Yuda, ndi okhala
m'Yerusalemu. 33Ndipo anandipatsa Ine mbuyo, si nkhope,
ngakhale ndinawaphunzitsa, kuuka m'mamawa ndi kuwaphunzitsa,
koma sanamvera kulangizidwa. 34Koma anaika zonyansa zao
m'nyumba yochedwa dzina langa, kuti aidetse. 35Ndipo anamanga
misanje ya Baala, iri m'cigwaca mwana wace wa Hinomu, kuti
apitirize kumoto ana ao amuna ndi akazi cifukwa ca Moleki; cimene
sindinauza, cimene sicinalowa m'mtima mwanga, kuti acite
conyansa ici, cocimwitsa Yuda.
36Cifukwa cace tsopano atero Yehova, Mulungu wa Israyeli, za
mudzi umene, munena inu, waperekedwa m'dzanja la mfumu ya
Babulo ndi lupanga, ndi njala, ndi caola: 37Taonani,
ndidzawasokolotsa m'maiko monse, kumene ndinawapitikitsira ndi
mkwiyo wanga, ndi m'kupsa mtima kwanga, ndi mu ukali waukuru,
ndipo ndidzawabwezeranso kumalo kuno, ndipo
ndidzawakhazikitsa mokhulupirika, 38ndipo adzakhala anthu anga,
ndipo Ine ndidzakhala Mulungu wao; 39ndipo ndidzawapatsa mtima
umodzi ndi njira imodzi, kuti andiope Ine masiku onse; kuwacitira
zabwino, ndi ana ao pambuyo pao; 40ndipo ndidzapangana nao
pangano lamuyaya, kuti sindidzawacokera kuleka kuwacitira
zabwino; koma ndidzalonga kuopsa kwanga m'mitima yao, kuti
asandicokere. 41Inde, ndidzasekerera iwo kuwacitira zabwino,
ndipo ndidzawaoka ndithu m'dziko lino ndi mtima wanga wonse ndi
moyo wanga wonse. 42Pakuti atero Yehova: Monga ndatengera
anthu awa coipa conseci, comweco ndidzatengera iwo zabwino
zonse ndawalonieza. 43Ndipo minda idzagulidwa m'dziko lino,
limene muti, Ndilo bwinja, lopanda munthu kapena nyama;
loperekedwa m'dzanja la Akasidi. 44Anthu adzagula minda ndi
ndalama, adzalembera akalata ogulira, adzawasindikiza, adzaitana
mboni, m'dziko la Benjamini, ndi m'malo ozungulira Yerusalemu,
ndi m'midzi ya Yuda, ndi m'midzi ya kumtunda, ndi m'midzi ya
kucidikha, ndi m'midzi ya ku Mwera; pakuti ndidzabweza undende
wao, ati Yehova.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Yehova abwereza kunena kuti anthu ace adzakhazikikanso m'dziko mwao, padzakhalanso mphukira

1Ndipo mau a Yehova anadza kwa Yeremiya nthawi yaciwiri,
pamene iye anali citsekedwere m'bwalo la kaidi, kuti, 2Atero
Yehova wocita zace, Yehova wolenga zace kuti azikhazikitse; dzina
lace ndi Yehova: 3Undiitane Ine, ndipo Ine ndidzakuyankha iwe,
ndipo ndidzakusonyeza iwe zazikuru, ndi zolakika, zimene
suzidziwa. 4Pakuti atero Yehova, Mulungu wa Israyeli, za nyumba
za mudzi uno, ndi za nyumba za mafumu a Yuda'zi, zinagwetsedwa
ziwacinjirizire mitumbira, ndi lupanga: 5Adza kumenyana ndi
Akasidi, koma adzangozidzaza ndi mitembo ya anthu, amene
ndawapha m'mkwiyo wanga ndi mu ukali wanga, amene ndabisira
mudzi uno nkhope yanga cifukwa ca zoipa zao zonse. 6Taonani,
ndidzautengera moyo ndi kuuciritsa, ndi kuwaciritsa; ndipo
ndidzawaululira iwo kucuruka kwa mtendere ndi zoona. 7Ndipo
ndidzabweza undende wa Yuda ndi wa Israyeli, ndipo
ndidzamangitsa mudzi wao, monga poyamba paja, 8Ndipo
ndidzawayeretsa kucotsa mphulupulu yao, imene anandicimwira
Ine; ndipo ndidzakhululukira mphulupulu zao zimene
anandicimwira, nandilakwira Ine. 9Ndipo ndidzayesa mudzi uno
cifukwa ca kukondwa, ndi ciyamiko ndi ulemerero, pamaso pa
amitundu onse a pa dziko lapansi, amene adzamva zabwino zonse
ndidzawacitirazo, ndipo adzaopa nadzanthunthumira cifukwa ca
zabwino zonse ndi mtendere wonse zimene ndidzaucitira. 10Atero
Yehova: M'malo muno, m'mene muti, Ndi bwinja, mopanda
munthu, mopanda nyama, m'midzi ya Yuda, m'makwalala a
Yerusalemu, amene ali bwinja, opanda munthu, opanda
wokhalamo, opanda nyama, 11mudzamvekanso mau akukondwa
ndi mau akusekera, mau a mkwati ndi mau a mkwatibwi, mau a
iwo akuti, Myamikireni Yehova wa makamu, pakuti Yehova ndiye
wabwino, cifundo cace ncosatha; ndi a iwo akutengera nsembe
zoyamikira m'nyumba ya Yehova. Pakuti ndidzabweza undende wa
dziko monga poyamba, ati Yehova. 12Yehova wa makamu atero:
M'malo muno, muli bwinja, mopanda munthu ndi nyama, m'midzi
yace yonse, mudzakhalanso mokhalamo abusa ogonetsa zoweta
zao. 13M'midzi ya kumtunda, m'midzi ya kucidikha, m'midzi ya ku
Mwera, m'dziko la Benjamini, m'malo ozungulira Yerusalemu,
m'midzi ya Yuda, zoweta zidzapitanso pansi pa manja a iye amene
aziwerenga, ati Yehova.
14Taonani, masiku alinkudza, ati Yehova, ndidzakhazikitsa mau
abwino aja ndinanena za nyumba ya Israyeli ndi za nyumba ya
Yuda. 15Masiku aja, nthawi ija, ndidzamphukitsira Davide mphukira
ya cilungamo; ndipo adzacita ciweruzo ndi cilungamo

m'dzikomu. 16Masiku omwewo Yuda adzapulumutsidwa, ndi
Yerusalemu adzakhala mokhulupirika; ili ndi dzina adzachedwa
nalo, Yehova ndiye cilungamo cathu. 17Pakuti Yehova atero: Davide
sadzasowa munthu wokhala pa mpando wacifumu wa nyumba ya
Israyeli; 18ndiponso ansembe sadzasowa munthu pamaso panga
wakupereka nsembe zopsereza, ndi kutentha nsembe zaufa, ndi
wakucita nsembe masiku onse. 19Ndipo mau a Yehova anadza kwa
Yeremiya, kuti, 20Ngati mukhoza kuswa pangano langa la usana ndi
pangano langa la usiku, kuti usakhalenso usana ndi usiku
m'nyengo yao; 21pamenepo pangano langa lidzasweka ndi Davide
mtumiki wanga, kuti asakhale ndi mwana wamwamuna
wakulamulira pa mpando wa ufumu wace; ndiponso ndi Alevi
ansembe, atumiki anga. 22Monga khamu la kuthambo silingathe
kuwerengedwa, ndi mcenga wa kunyanja sungathe kuyesedwa;
comweco ndidzacurukitsa mbeu za Davide mtumiki wanga, ndi
Alevi akunditumikira Ine. 23Ndipo mau a Yehova anadza kwa
Yeremiya, kuti, 24Kodi sulingalira comwe anena anthu awa, kuti,
Mabanja awiri amene Yehova anawasankha, wataya iwo? comweco
anyoza anthu anga, kuti asakhalenso mtundu pamaso
pao. 25Yehova atero: Likaleka kukhala pangano langa la usana ndi
usiku, ngati sindinalemba malemba a kumwamba ndi dziko
lapansi; 26pamenepo ndidzatayanso mbeu ya Yakobo, ndi ya
Davide mtumiki wanga, kuti sindidzatenganso za mbeu zace kuti
zikhale zolamulira mbeu za Abrahamu, ndi za Isake, ndi za Yakobo;
pakuti ndidzabweundende wao, ndipo ndidzawacitira cifundo.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Yeremiya 34

Zedekiya adzatengedwa, Yerusalemu adzalandidwa
1Mau amene anadza kwa Yeremiya kucokera kwa Yehova, pamene
Nebukadinezara mfumu ya Babulo, ndi nkhondo yace yonse, ndi maufumu
onse a dziko lapansi amene anagwira mwendo wace, ndi anthu onse,
anamenyana ndi Yerusalemu, ndi midzi yace yonse, akuti: 2Yehova Mulungu
wa Israyeli atero, Pita, nena kwa Zedekiya mfumu ya Yuda, numuuze iye, kuti
Yehova atero, Taona, ndidzapereka mudziwu m'dzanja la mfumu ya ku Babulo,
ndipo adzautentha ndi moto; 3ndipo iwe sudzapulumuka m'dzanja lace, koma
udzagwiridwadi, nudzaperekedwa m'dzanja lace; ndipo maso ako adzaanana
nao a mfumu ya ku Babulo, ndipo iye adzanena nawe pakamwa ndi pakamwa,
ndipo udzanka ku Babulo. 4Koma tamva mau a Yehova, iwe Zedekiya mfumu
ya Yuda; Yehova atero za iwe, Sudzafa ndi lupanga; 5udzafa ndi mtendere;
ndipo adzawambika iwe monga anawambika makolo ako, mafumu akale
usanakhale iwe; ndipo adzakulirira iwe, kuti, Kalanga ine ambuye! pakuti
ndanena mau, ati Yehova. 6Ndipo Yeremiya mneneri ananena mau onsewa
kwa Zedekiya mfumu ya Yuda m'Yerusalemu, 7pamene nkhondo ya mfumu ya
ku Babulo inamenyana ndi Yerualemu, ndi midzi yonse ya Yuda imene
inatsala, ndi Lakisi ndi Azeka; pakuti midzi ya Yuda yamalinga yotsala ndi
imeneyi.

Oyesa abale ao akapolo aopsedwa

8Mau amene anadza kwa Yeremiya kucokera kwa Yehova, atapangana
Zedekiya pangano ndi anthu onse amene anali pa Yerusalemu, kuti awalalikire
iwo ufulu; 9kuti yense ammasule kapolo wace wamwamuna, ndi wamkazi,
pokhala iye Mhebri wamwamuna kapena wamkazi, kuti yense asayese Myuda
mnzace kapolo wace; 10ndipo akuru onse ndi anthu onse anamvera, amene
anapangana mapangano, akuti yense ammasule kapolo wace wamwamuna,
kapena wamkazi osawayesanso akapolo; iwo anamvera nawamasula; 11koma
pambuyo pace anabwerera, nabweza akapolo ace amuna ndi akazi, amene
anawamasula, nawagonjetsanso akhale akapolo amuna ndi akazi; 12cifukwa
cace mau a Yehova anadza kwa Yeremiya kucokera kwa Yehova,
kuti, 13Yehova Mulungu wa Israyeli atero: Ndinapangana mapangano ndi
makolo anu tsiku lija ndinawaturutsa m'dziko la Aigupto, kuturuka m'nyumba
ya ukapolo, kuti, 14Zitapita zaka zisanu ndi ziwiri mudzaleka amuke yense
mbale wace amene ali Mhebri, amene anagulidwa ndi inu, amene
anakutumikirani inu zaka zisanu ndi cimodzi, mudzammasule akucokereni;
koma makolo anu sanandimvera Ine, sanandichera Ine khutu, 15Ndipo
mwabwerera inu tsopano, ndi kucita cimene ciri colungama pamaso panga,
pakulalikira ufulu yense kwa mnzace; ndipo munapangana pangano pamaso
panga m'nyumba imene ichedwa dzina langa; 16koma mwabwerera ndi
kuipitsa dzina langa, ndi kubwezera m'ukapolo yense kapolo wace
wamwamuna, ndi wamkazi, amene munammasula akacite zao, ndipo
munawagonjetsa, akhale akapolo anu amuna ndi akazi. 17Cifukwa cace
Yehova atero: Simunandimvera Ine, kuti mulalikire ufulu, munthu yense kwa
mbale wace, ndi munthu yense kwa mnzace; taonani, ndilalikira kwa inu
ufulu, ati Yehova, wa kulupanga, kucaola, ndi kunjala; ndipo ndidzakuperekani
mukhale oopsetsa m'maufumu onse a dziko lapansi. 18Ndipo ndidzapereka
anthu akulakwira pangano langa, amene sanacita mau a pangano limene
anapangana pamaso panga, muja anadula pakati mwana wa ng'ombe ndi
kupita pakati pa mbali zace; 19akulu a Yuda, ndi akulu a Yerusalemu, adindo,
ndi ansembe, ndi anthu onse a m'dziko, amene anapita pakati pa mbali za

mwana wa ng'ombe; 20ndidzapereka iwo m'dzanja la adani ao, ndi m'dzanja
la iwo akufuna moyo wao; ndipo mitembo yao idzakhala cakudya ca mbalame
za mlengalenga, ndi ca zirombo za pa dziko lapansi. 21Ndipo Zedekiya mfumu
ya Yuda ndi akulu ace ndidzawapereka m'dzanja la adani ao, ndi m'dzanja la
akufuna moyo wao, ndi m'dzanja la nkhondo ya mfumu ya ku Babulo, imene
yakucokerani. 22Taonani, ndidzauza, ati Yehova, ndidzabwezera iwo ku mudzi
uno; ndipo adzamenyana nao, nadzaulanda, nadzautentha ndi moto; ndipo
ndidzayesa midzi ya Yuda mabwinja, palibenso wokhalamo.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Kukhulupirika kwa Arekabu kukhale citsanzo ca kwa Yuda

1Mau amene anadza kwa Yeremiya kucokera kwa Yehova masiku a
Yehoyakimu mwana wa Yosiya, mfumu ya Yuda, kuti, 2Pita ku
nyumba ya Arekabu, nunene nao, nulowetse iwo m'nyumba ya
Yehova, m'cipinda cina, nuwapatse iwo vinyo amwe. 3Ndipo
ndinatenga Yaasaniya mwana wa Yeremiya, mwana wa Habazinya,
ndi abale ace, ndi ana amuna ace, ndi nyumba yonse ya
Arekabu; 4ndipo ndinawalowetsa m'nyumba ya Yehova, m'cipinda
ca ana a Hanani mwana wa Igadaliya, munthu wa Mulungu,
cokhala pambali pa cipinda ca akuru, ndico cosanjika pa cipinda ca
Maseya mwana wa Salumu, mdindo wa pakhomo; 5ndipo ndinaika
pamaso pa ana amuna a nyumba ya Arekabu mbale zodzala ndi
vinyo, ndi zikho, ndipo ndinati kwa iwo, Imwani vinyo. 6Koma anati,
Sitidzamwa vinyo; pakuti Yonadabu mwana wa Rekabu kholo lathu
anatiuza ife, kuti, Musadzamwe vinyo, kapena inu, kapena ana
anu, kumuyaya; 7ndiponso musamange nyumba, musafese mbeu,
musaoke mipesa, musakhale nayo; koma masiku anu onse
mudzakhale m'mahema; kuti mukhale ndi moyo masiku ambiri
m'dziko limene mukhalamo alendo. 8Ndipo ife tamva mau a
Yonadabu mwana wa Rekabu kholo lathu m'zonse zimene anatiuza
ife, zakuti tisamwe vinyo masiku athu onse, ife, akazi athu, ana
athu amuna ndi akazi; 9ngakhale kudzimangira nyumba
zokhalamo; ndipo sitiri nao munda wamphesa, kapena munda,
kapena mbeu; 10koma takhala m'mahema, ntimvera, nticita
monga mwa zonse anatiuza Yonadabu kholo lathu. 11Koma panali,
pamene Nebukadirezara mfumu ya ku Babulo anadza m'dzikomu,
ife tinati, Tiyeni tinke ku Yerusalemu cifukwa tiopa nkhondo ya
Akasidi, ndi nkhondo ya Aramu; ndipo tikhala m'Yerusalemu.
12Ndipo anadza mau a Yehova kwa Yeremiya, kuti, 13Atero Yehova
wa makamu, Mulungu wa Israyeli: Pita, nunene kwa anthu a Yuda
ndi kwa okhala m'Yerusalemu, Kodi simudzalola kulangizidwa
kumvera mau anga ati Yehova. 14Mau a Yonadabu mwana wa
Rekabu, amene anauza ana ace, asamwe vinyo, alikucitidwa, ndipo
mpaka lero samamwa, pakuti amvera lamulo la kholo lao; koma
Ine ndanena ndi inu, ndalawirira ndi kunena; koma
simunandimvera Ine. 15Ndatumanso kwa inu atumiki anga onse
aneneri, ndalawirira ndi kuwatuma, kuti, Bwererani kuleka yense
njira yace yoipa, konzani macitidwe anu, musatsate milungu yina
kuitumikira, ndipo mudzakhala m'dziko limene ndakupatsani inu
ndi makolo anu; koma simunandichera khutu lanu,
simunandimvera Ine. 16Pakuti monga ana a Yonadabu mwana wa
Rekabu acita lamulo la kholo lao limene anawauza, koma anthu
awa sanandimvera Ine. 17Cifukwa cace atero Yehova, Mulungu wa

makamu, Mulungu wa Israyeli: Taonani, ndidzafikitsa pa Yuda ndi
pa onse okhala m'Yerusalemu coipa conseco ndawanenera iwo;
cifukwa ndanena ndi iwo, koma sanamve; ndaitana, koma iwo
sanandibvomera. 18Ndipo Yeremiya anati kwa nyumba ya Arekabu,
Atero Yehova wa makamu, Mulungu wa Israyeli: Cifukwa
mwamvera lamulo la Yonadabu kholo lanu, ndi kusunga zonse
anakulangizani inu, ndi kucita monga mwa zonse anakuuzani
inu; 19cifukwa cace atero Yehova wa makamu, Mulungu wa Israyeli:
Yonadabu mwana wa Rekabu sadzasowa munthu wakuima pamaso
panga kumuyaya.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Mau a Yeremiya alembedwa pampukutu nawerengedwa m'Kacisi, natenthedwa ndi mfumu

1Ndipo panali caka cacinai ca Yehoyakimu mwana wa Yosiya,
mfumu ya Yuda, mau awa anadza kwa Yeremiya kucokera kwa
Yehova, kuti, 2Tenga buku lampukutu, nulembe m'menemo mau
onse ndanena kwa iwe akunenera Israyeli, ndi akunenera Yuda, ndi
akunenera amitundu onse, kuyambira tsiku ndinanena kwa iwe,
kuyambira masiku a Yosiya, mpaka lero. 3Kapena nyumba ya Yuda
idzamva coipa conse cimene nditi ndidzawacitire; kuti abwerere
yense kuleka njira yace yoipa; kuti ndikhululukire mphulupulu yao
ndi cimo lao. 4Ndipo Yeremiya anaitana Baruki mwana wa Neriya;
ndipo Yeremiya analembetsa Baruki m'buku lampukutu mau onse a
Yehova, amene ananena naye. 5Ndipo Yeremiya anauza Baruki,
kuti, Ndaletsedwa sindithai kulowa m'nyumba ya Yehova; 6koma
pita iwe, nuwerenge mu mpukutu umene ndakulembetsa, mau a
Yehova m'makutu a anthu m'nyumba ya Yehova tsiku lakusala
kudya; ndiponso udzawawerenga m'makutu a Ayuda onse amene
aturuka m'midzi yao. 7Kapena pembedzero lao lidzagwa pamaso
pa Yehova, ndipo adzabwerera yense kuleka njira yace yoipa;
pakuti mkwiyo ndi ukali umene Yehova wanenera anthu awa ndi
waukuru. 8Ndipo Baruki mwana wa Neriya anacita monga mwa
zonse anamuuza iye Yeremiya mneneri, nawerenga m'buku mau a
Yehova m'nyumba ya Yehova.
9Ndipo panali caka cacisanu ca Yehoyakimu mwana wa Yosiya,
mfumu ya Yuda, mwezi wacisanu ndi cinai, anthu onse a
m'Yerusalemu, ndi anthu onse ocokera m'midziya Yuda kudzaku
Yerusalemu, analalikira kusala kudya pamaso pa Yehova. 10Ndipo
Baruki anawerenga m'buku mau a Yeremiya m'nyumba ya Yehova,
m'cipinda ca Gemariya mwana wa Safani mlembi, m'bwalo la
kumtunda, pa khomo la cipata catsopano ca nyumba ya Yehova,
m'makutu a anthu onse. 11Pamene Mikaya mwana wa Hemariya,
mwana wa Safani, anamva m'buku mau onse a
Yehova, 12anatsikira ku nyumba ya mfumu, nalowa m'cipinda ca
mlembi; ndipo, taonani, akuru onse analikukhalamo, Elisama
mlembi, ndi Delaya mwana wa Semaya, ndi Elinatani mwana wa
Akibori, ndi Gemariya mwana wa Safani, ndi Zedekiya mwana wa
Hananiya, ndi akuru onse. 13Ndipo Makaya anafotokozera iwo mau
onse amene anamva, pamene Baruki anawerenga buku m'makutu
a anthu. 14Cifukwa cace akuru onse anatuma Yehudi mwana wa
Nataniya, mwana wa Salamiya, mwana wa Kusa, kwa Baruki,
kukanena, Tenga m'dzanja lako mpukutu wauwerenga m'makutu a
anthu, nudze kuno. Ndipo Baruki mwana wa Neriya anatenga
mpukutuwo m'dzanja lace, nadza kwa iwo. 15Ndipo anati kwa iye,

Khala pansi tsopano, nuwerenge m'makutu athu. Ndipo Baruki anauwerenga m'makutu ao. 16Ndipo panali, pamene anamva mau onse, anaopa nayang'anana wina ndi mnzace, nati kwa Baruki, Tidzamfotokozeratu mfumu mau awa onse. 17Ndipo anamfunsa Baruki, kuti, Utifotokozeretu, Unalemba bwanji mau awa onse ponena iye? 18Ndipo Baruki anayankha iwo, Pakamwa pace anandichulira ine mau awa onse, ndipo ndinawalemba ndi inki m'bukumo. 19Ndipo akuru anati kwa Baruki, Pita, nubisale iwe ndi Yeremiya; munthu yense asadziwe kumene muli. 20Ndipo analowa kwa mfumu kubwalo; ndipo anasunga buku m'cipinda ca Elisama mlembi; nafotokozera mau onse m'makutu a mfumu. 21Ndipo mfumu anatuma Yehudi atenge mpukutuwo; ndipo anautenga kuturuka nao m'cipinda ca Elisama mlembi, Ndipo Yehudi anauwerenga m'makutu a mfumu, ndi m'makutu a akuru onse amene anaima pambali pa mfumu. 22Ndipo mfumu anakhala m'nyumba ya nyengo yacisanu mwezi wacisanu ndi cinai; ndipo munali moto m'nkhumbaliro pamaso pace. 23Ndipo panali, pamene Yehudi anawerenga masamba atatu pena anai, mfumu inawadula ndi kampeni ka mlembi, niwaponya m'moto wa m'nkhumbaliromo, mpaka mpukutu wonse unatha kupsa ndi moto wa m'nkhumbaliromo. 24Ndipo sanaopa, sanang'ambe nsaru zao, kapena mfumu, kapena atumiki ace ali yense amene anamva mau onsewa. 25Tsononso Elinatani ndi Deliya ndi Gemariya anapembedzera mfumu kuti asatenthe mpukutuwo; koma anakana kumvera. 26Ndipo mfumu inauza Yeremeeli mwana wace wa mfumu, ndi Seraya mwana wa Azirieli, ndi Selemiya mwana wa Abidieli, kuti awagwire Baruki mlembi ndi Yeremiya mneneri; koma Yehova anawabisa.
27Ndipo mau a Yehova anadza kwa Yeremiya, mfumu itatentha mpukutuwo, ndi mau amene analemba Baruki ponena Yeremiya, kuti, 28Tenganso mpukutu wina, nulembe m'menemo mau oyamba aja anali mu mpukutu woyamba uja, umene Yehoyakimu mfumu ya Yuda wautentha. 29Ndipo za Yehoyakimu mfumu ya Yuda uziti, Yehova atero: Iwe watentha mpukutu uwu, ndi kuti, Bwanji walemba m'menemo, kuti, Mfumu ya ku Babulo idzadzadi nidzaononga dziko ili, nidzatha m'menemo anthu ndi nvama? 30Cifukwa cace Yehova atero za Yehoyakimu mfumu ya Yuda: Adzasowa wokhala pa mpando wacifumu wa Davide; ndipo mtembo wace udzaponyedwa usana kunja kuli dzuwa, ndi usiku kuli cisanu. 31Ndipo ndidzamlanga iye ndi mbeu zace ndi atumiki ace cifukwa ca mphulupulu zao; ndipo ndidzawatengera iwo, ndi okhala m'Yerusalemu, ndi anthu a Yuda, zoipa zonse ndawanenera iwo, koma sanamvera. 32Ndipo Yeremiya anatenga mpukutu wina, naupereka kwa Baruki mlembi, mwana wa Neriya; amene

analemba m'menemo ponena Yeremiya mau onse a m'buku lija Yehoyakimu mfumu ya Yuda analitentha m'moto; ndipo anaonjezapo mau ambiri oterewa.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Yeremiya m'kaidi

1Ndipo Zedekiya mwana wa Yosiya anakhala mfumu m'malo a
Koniya mwana wa Yehoyakimu, amene Nebukadirezara mfumu ya
ku Babulo inamlowetsa mfumu m'dziko la Yuda. 2Koma ngakhale
iye, ngakhale atumiki ace, ngakhale anthu a padziko, sanamvere
mau a Yehova, amene ananena mwa Yeremiya mneneri.
3Ndipo Zedekiya mfumu anatuma Yehukali mwana wa Selemiya,
ndi Zefaniya mwana wa Maseya wansembe, kwa Yeremiya
mneneri, kukanena, Mutipempherereretu kwa Yehova Mulungu
wathu. 4Ndipo Yeremiya analikuyendayenda mwa anthu; cifukwa
asanamuike iye m'nyumba yandende. 5Ndipo nkhondo ya Farao
inaturuka m'Aigupto; ndipo pamene Akasidi omangira misasa
Yerusalemu anamva mbiri yao, anacoka ku Yerusalemu. 6Ndipo
mau a Yehova anadza kwa Yeremiya mneneri, kuti, 7Atero Yehova,
Mulungu wa Israyeli: Muzitero kwa mfumu ya Yuda, imene
inakutumani inu kwa Ine kuti mundifunse Ine: Taonani, nkhondo ya
Farao, yakuturukira kudzathandiza inu, idzabwerera ku Aigupto ku
dziko lao. 8Ndipo Akasidi adzabweranso, nadzamenyana ndi mudzi
uwu; ndipo adzaulanda, nadzautentha ndi moto. 9Yehova atero:
Musadzinyenge, kuti, Akasidi adzaticokera ndithu; pakuti
sadzacoka. 10Pakuti ngakhale mukadakantha nkhondo yonse ya
Akasidi akumenyana, nanu, ngakhale akadatsala olasidwa okha
okha mwa iwo, koma iwowa akadauka yense m'hema wace ndi
kutentha mudzi uwu ndi moto.
11Ndipo panali pamene nkhondo ya Akasidi inacoka ku Yerusalemu
cifukwa ca nkhondo ya Farao, 12pamenepo Yeremiya anaturuka
m'Yerusalemu kumuka ku dziko la Benjamini, kukalandira gawo
lace kumeneko. 13Pokhala iye m'cipinda ca Benjamini, kapitao wa
alonda anali kumeneko, dzina lace Iriya, mwana wa Selemiya,
mwana wa Hananiya; ndipo iye anamgwira Yeremiya mneneri, nati,
Ulinkupandukira kwa Akasidi. 14Ndipo anati Yeremiya, Kunama
kumeneko; ine sindipandukira kwa Akasidi; koma sanamvera iye;
ndipo Iriya anamgwira Yeremiya, nanka naye kwa akuru. 15Ndipo
akuru anakwiyira Yeremiya, nampanda iye, namuika m'nyumba
yandende m'nyumba ya Yonatani mlembi; pakuti anaiyesa
ndende. 16Atafika Yeremiya ku nyumba yadzenje, ku tizipinda tace
nakhalako Yeremiya masiku ambiri; 17pamenepo Zedekiya mfumu
inatuma, ndi kumtenga iye; ndipo mfumu inamfunsa iye m'tseri
m'nyumba mwace, niti, Kodi alipo mau ocokera kwa Yehova? Ndipo
Yeremiya, anati, Alipo, Anatinso, Mudzaperekedwa m'dzanja la
mfumu ya ku Babulo. 18Ndipo Yeremiya anati kwa mfumu
Zedekiya, Ndacimwira inu ciani, kapena atumiki anu, kapena anthu
awa, kuti mwandiika m'nyumba yandende? 19Tsopano ali kuti

aneneri anu, amene ananenera inu, kuti, Mfumu ya ku Babulo
sidzakudzerani inu, kapena dziko lino? 20Tsopano tamvanitu,
mbuyanga mfumu; pembedzero langa ligwe pamaso panu; kuti
musandibwezere ku nyumba ya Yonatani mlembi, ndingafe
kumeneko. 21Ndipo Zedekiya mfumu analamula, ndipo anamuika
Yeremiya m'bwalo la kaidi, tsiku ndi tsiku, nampatsa mkate
wofuma ku mseu wa oumba mikate, mpaka unatha mkate wonse
wa m'mudzi. Ndipo Yeremiya anakhala m'bwalo la kaidi.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Yeremiya aponyedwa m'dzenje muli thope

1Ndipo Sefatiya mwana wa Matani ndi Gedaliya mwana wa Pusuri,
ndi Yukali mwana wa Selemiya, ndi Pasuri mwana wa Malikiya,
anamva mau amene Yeremiya ananena ndi anthu onse,
kuti, 2Yehova atero, Iye wakukhala m'mudziwu adzafa ndi lupanga,
ndi njala, ndi caola; koma iye wakuturukira kunka kwa Akasidi
adzakhala ndi moyo, ndipo adzakhala nao moyo wace ngati
cofunkha, nadzakhala ndi moyo. 3Yehova atero, Mudziwu
udzapatsidwatu m'dzanja la nkhondo ya mfumu ya ku Babulo,
ndipo adzaulanda. 4Ndipo akuru anati kwa mfumu, Munthu uyu
aphedwetu; cifukwa analopetsa manja a anthu a nkhondo otsala
m'mudzi uno, ndi manja a anthu onse, pakunena kwa iwo mau
otero; pakuti munthu uyu safuna mtendere wa anthu awa, koma
nsautso yao. 5Ndipo mfumu Zedekiya anati, Taonani, ali m'manja
mwanu; pakuti mfumu singathe kucita kanthu kotsutsana
nanu. 6Ndipo anatenga Yeremiya, namponya iye m'dzenje la
Malikiya mwana wace wa mfumu, limene linali m'bwalo la kaidi;
ndipo anamtsitsa Yeremiya ndi zingwe, Koma m'dzenjemo
munalibe madzi, koma thope; namira Yeremiya m'thopemo. 7Ndipo
pamene Ebedi-Meleki Mkusi, mdindo, anamva kuti anamuika
Yeremiya m'dzenje; mfumu irikukhala pa cipata ca
Benjamini; 8Ebedi-Meleki anaturuka m'nyumba ya mfumu, nanena
ndi mfumu, kuti, 9Mbuyanga mfumu, anthu awa anacita zoipa
m'zonse anacitira Yeremiya mneneri, amene anamponya m'dzenje;
ndipo afuna kufa m'menemo cifukwa ca njala; pakuti mulibe
cakudya cina m'mudzimu. 10Ndipo mfumu inamuuza Ebedi-Meleki
Mkusi, kuti, Tenga anthu makumi atatu, umkweze numturutse
Yeremiya mneneri m'dzenjemo, asanafe. 11Ndipo Ebedi-Meleki
anatenga anthuwo, nalowa nao m'nyumba ya mfumu ya pansi pa
nyumba ya cuma, natenga m'menemo nsaru zakale zotaya ndi
zansanza zobvunda, nazitsitsira ndi zingwe kwa Yeremiya
m'dzenjemo. 12Ndipo Ebedi-Meleki Mkusi anati kwa Yeremiya,
Kulungatu zingwe ndi nsaruzi zotaya zakale ndi zansanza ndi
kuzikwapatira. Ndipo Yeremiya anacita comweco. 13Ndipo
anamkweza Yeremiya ndi zingwe, namturutsa m'dzenjemo; ndipo
Yeremiya anakhalabe m'bwalo la kaidi.
14Ndipo mfumu Zedekiya anatuma, natntenga Yeremiya mneneri
nalowa naye m'khomo lacitatu la nyumba ya Yehova; ndipo mfumu
inati kwa Yeremiya, Ndidzakufunsa iwe kanthu; usandibisire ine
kanthu. 15Ndipo Yeremiya anati kwa Zedekiya,
Ndikakufotokozerani, kodi simudzandipha ine? ndipo
ndikakupangirani, simudzandimveta ine. 16Ndipo Zedekiya
analumbira m'tseri kwa Yeremiya, kuti, Pali Yehova, amene

anatilengera ife moyo uno, sindidzakupha iwe sindidzakupereka iwe m'manja mwa anthu awa amene afuna moyo wako. 17Ndipo Yeremiya anati kwa Zedekiya, Atero Yehova, Mulungu wa makamu, Mulungu wa Israyeli: Ngati mudzaturukira kwa akuru a mfumu ya ku Babulo, mudzakhala ndi moyo, ndipo mudziwu sudzatenthedwa ndi moto; ndipo mudzakhala ndi moyo ndi banja lanu; 18koma ngati simudzaturukira kwa akuru a mfumu ya ku Babulo, mudziwu udzaperekedwa m'dzanja la Akasidi, ndipo udzatenthedwa ndi moto, ndipo simudzapulumuka m'manja mwao. 19Ndipo mfumu Zedekiya anati kwa Yeremiya, Ine ndiopa Ayuda amene anandipandukira ine kunka kwa Akasidi, angandipereke ine m'manja mwao, angandiseke. 20Koma Yeremiya anati, Sadzakuperekani. Mveranitu mau a Yehova, amene ndinena ndi inu, comweco kudzakomera inu, ndipo moyo wanu udzakhalabe. 21Koma ngati mukana kuturuka, mau anandisonyeza Yehova ndi awa: 22Taonani, akazi onse otsala m'nyumba ya mfumu ya Yuda adzaturutsidwa kunka kwa akuru a mfumu ya ku Babulo, ndipo akaziwo adzati, Oyanjana nanu anakunyengani, ndi kukuposani inu, mapazi anu amire m'thope, abwerera m'mbuyo. 23Ndipo adzaturutsira Akasidi akazi anu onse, ndi ana anu, ndipo simudzapulumuka m'manja ao, koma mudzagwidwa ndi dzanja la mfumu ya ku Babulo; ndipo mudzatenthetsa mudziwu ndi moto. 24Ndipo Zedekiya anati kwa Yeremiya, Anthu asadziwe mau amene, ndipo sudzafa. 25Koma akamva akuru kuti ndalankhula ndi iwe, nakafika kwa iwe, ndi kuti kwa iwe, Utifotokozere ife comwe wanena kwa mfumu; osatibisira ici, ndipo sitidzakupha iwe; ndiponso zomwe mfumu inanena kwa iwe; 26pamenepo uziti kwa iwo, Ndinagwa ndi pembedzero langa pamaso pa mfumu, kuti asandibwezerenso ku nyumba ya Yonatani ndifere komweko. 27Ndipo akuru onse anadza kwa Yeremiya, namfunsa; ndipo iye ananena nao monga mwa mau onsewo anamuuza mfumu. Ndipo analeka kunena naye; pakuti sikunamveka mlandu. 28Ndipo Yeremiya anakhala m'bwalo la kaidi mpaka dzuwa lakugwidwa Yerusalemu. Ndipo anali komweko pogwidwa Yerusalemu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Nebukadirezara alanda Yerusalemu, nalanditsa Yeremiya

1Caka cacisanu ndi cinai ca Zedekiya mfumu ya Yuda, mwezi
wakhumi, anadza Nebukadirezara mfumu ya ku Babulo ndi
nkhondo yace yonse, ndi kuumangira misasa. 2Caka cakhumi ndi
cimodzi ca Zedekiya, mwezi wacinai, tsiku lacisanu ndi cinai, mudzi
unabooledwa. 3Ndipo akuru onse a mfumu ya ku Babulo analowa,
nakhala m'cipata capakati, Nerigalisarezara, Samgari Nebo,
Sarisekimu, mkuru wa adindo, Nerigalisarezara mkuru wa alauli ndi
akuru ena onse a mfumu ya ku Babulo. 4Ndipo panali pamene
Zedekiya mfumu ya Yuda ndi amuna onse a nkhondo anawaona,
anathawa naturuka m'mudzi usiku, panjira pa munda wa mfumu,
pa cipata ca pakati pa makoma awiri; ndipo iye anaturukira pa
njira ya kucidikha. 5Koma nkhondo ya Akasidi inawalondola,
nimpeza Zedekiya m'zidikha za Yeriko; ndipo atamgwira,
anamtengera kwa Nebukadirezara mfumu ya ku Babulo ku Ribila
m'dziko la Hamati, ndipo iye ananena naye mlandu. 6Pamenepo
mfumu ya ku Babulo inapha ana a Zedekiya ku Ribila pamaso
pace; mfumu ya ku Babulo niphanso aufulu onse a Yuda. 7Ndipo
anakolowola maso a Zedekiya, nammanga m'zigologolo, kunka
naye ku Babulo. 8Ndipo Akasidi anatentha ndi moto nyumba ya
mfumu, ndi nyumba za anthu, nagumula malinga a
Yerusalemu. 9Ndipo Nebuzaradani kapitao wa alonda anatenga
anthu otsalira m'mudzi, ndi othawa omwe, opandukira, ndi
kumtsata ndi anthu otsalira nanka nao am'nsinga ku
Babulo. 10Koma aumphawi a anthu, amene analibe kanthu,
Nebuzaradani kapitao wa alonda anawasiya m'dziko la Yuda,
nawapatsa mipesa ndi minda nthawi yomweyo. 11Ndipo
Nebukadirezara mfumu ya ku Babulo anamuuza Nebuzaradani
kapitao wa alonda, za Yeremiya, kuti, 12Umtenge, numyang'anire
bwino, usamsautse, koma umcitire monga iye adzanena
nawe. 13Ndipo Nebuzaradani kapitao wa alonda anatumiza, ndi
Nebusazibani, mkuru wa adindo Rabi-Sarisi, ndi Nerigalisarezari
mkuru wa alauli, ndi akuru onse a mfumu ya ku Babulo; 14iwonso
anatumiza, namcotsa Yeremiya m'bwalo la kaidi, nampereka iye
kwa Gedaliya mwana wa Ahikamu, mwana wa Safani, kuti anke
naye kwao; momwemo iye anakhala ndi anthu.
15Ndipo mau a Yehova anadza kwa Yeremiya, potsekeredwa iye
m'bwalo la kaidi, kuti, 16Pita, ukanene kwa Ebedi-Meleki Mkusi,
kuti, Atero Yehova wa makamu, Mulungu wa Israyeli: Taona,
ndidzafikitsira mudzi uwu mau anga kuusautsa, osaucitira zabwino;
ndipo adzacitidwa pamaso pako tsiku lomwelo. 17Koma
ndidzakupulumutsa tsiku lomwelo, ati Yehova: ndipo
sudzaperekedwa m'manja a anthu amene uwaopa. 18Pakuti

ndidzakupulumutsatu ndipo sudzagwa ndi lupanga, koma udzakhala nao moyo wako ngati cofunkha, pakuti wandikhulupirira Ine, ati Yehova.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Yeremiya apita kwa Gedaliya ku Mizipa

1Mau amene anadza kwa Yeremiya kucokera kwa Yehova,
Nebuzaradani kapitao wa alonda atammasula pa Rama, pamene
anamtenga iye womangidwa m'maunyolo pamodzi ndi am'nsinga
onse a Yerusalemu ndi Yuda, amene anatengedwa am'nsinga
kunka nao ku Babulo. 2Ndipo kapitao wa alonda anatenga
Yeremiya, nati kwa iye, Yehova Mulungu wako ananenera coipa ici
malo ano; 3ndipo Yehova wacitengera, ndi kucita monga ananena,
cifukwa mwacimwira Yehova, ndi kusamvera mau ace, cifukwa
cace cinthu ici cakufikirani. 4Ndipo tsopano, taona, ndikumasula
iwe lero maunyolo ali pa manja ako. Kukakukomera kudza nane ku
Babulo, idza, ndipo ndidzakusamalira bwino; koma kukakuipira
kudza nane ku Babulo, tsala; taona, dziko lonse liri pamaso pako;
kuli konse ukuyesa kwabwino kapena koyenera kupitako, pita
kumeneko. 5Tsono asanabwerere iye anati, Bweratu kwa Gedaliya
mwana wa Ahikamu, mwana wa Safani, amene mfumu ya ku
Babulo inamyesa wolamulira midzi ya Yuda, nukhale naye pakati
pa anthu; kapena pita kuli konse ukuyesa koyenera kupitako. Ndipo
kapitao wa alonda anampatsa iye phoso ndi mtulo, namleka
amuke. 6Ndipo Yeremiya ananka kwa Gedaliya mwana wa Ahikamu
ku Mizipa, nakhala kumeneko kwa anthu otsala m'dziko.
7Ndipo pamene akuru onse a makamu amene anali m'minda, iwo
ndi anthu ao, anamva kuti mfumu ya ku Babulo adamuika Gedaliya
mwana wa Ahikamu wolamulira dziko, nampatsira amuna, ndi
akazi, ndi ana, ndi aumphawi a m'dzikomo, a iwo amene
sanatengedwa ndende kunka nao ku Babulo; 8pamenepo anadza
kwa Gedaliya ku Mizipa, Ismayeli mwana wa Netaniya, ndi
Yohanani ndi Yonatani ana a Kareya, ndi Saraya mwana wa
Tanumeti, ndi ana a Efai wa ku Netofa, ndi Jezaniya mwana wa
munthu wa ku Maaka, iwo ndi anthu ao. 9Ndipo Gedaliya mwana
wa Ahikamu mwana wa Safani anawalumbirira iwo ndi anthu ao,
kuti, Musaope kuwatumikira Akasidi; khalani m'dzikomu,
mutumikire mfumu ya ku Babulo, ndipo kudzakukomerani. 10Koma
ine, taonani, ndidzakhala pa Mizipa, ndiima pamaso pa Akasidi,
amene adzadza kwa ife; koma inu, sonkhanitsani vinyo ndi zipatso
zamalimwe ndi mafuta, muziike m'mbiya zanu, nimukhale m'midzi
imene mwailanda. 11Comweco pamene Ayuda onse okhala
m'Moabu ndi mwa ana a Amoni, ndi m'Edomu, ndi amene anali
m'maiko monse, anamva kuti mfumu ya ku Babulo inasiya otsala a
Yuda, ndi kuti inamuika Gedaliya mwana wa Ahikamu, mwana wa
Safani wolamulira wao; 12pamenepo Ayuda onse anabwerera
kufumira ku malo onse kumene anawaingitsirako, nafika ku dziko

la Yuda, kwa Gedaliya, ku Mizipa, nasonkhanitsa vinyo ndi zipatso zamalimwe zambiri.
13Ndiponso Yohanani mwana wa Kareya, ndi akazembe onse a nkhondo okhala m'minda, anadza kwa Gedaliya ku Mizipa, 14nati kwa iye, Kodi mudziwa kuti Baalisi mfumu ya ana a Amoni watumiza Ismayeli mwana wa Netaniya kuti akupheni inu? Koma Gedaliya mwana wa Ahikamu sanamvera iwo. 15Ndipo Yohanani mwana wa Kareya ananena kwa Gedaliya m'tseri, kuti, Ndimuketu, ndikaphe Ismayeli mwana wa Netaniya, anthu osadziwa; cifukwa canji adzakuphani inu, kuti Ayuda onse amene anakusonkhanira inu amwazike, ndi otsala a Yuda aonongeke? 16Koma Gedaliya mwana wa Ahikamu anati kwa Yohanani mwana wa Kareya, Usacite ici; pakuti unamizira Ismayeli.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Gedaliya ndi ena aphedwa ndi Ismayeli

1Ndipo panali mwezi wacisanu ndi ciwiri, Ismayeli mwana wa
Netaniya, mwana wa Elisama, wa mbeu ya mfumu, ndi kapitao
wamkuru wa mfumu, ndi anthu khumi pamodzi ndi iye, anadza
kwa Gedaliya mwana wa Ahikamu ku Mizipa; pamenepo anadya
pamodzi m'Mizipa. 2Ndipo anauka Ismayeli mwana wa Netaniya,
ndi anthu khumi okhala naye, namkantha Gedaliya mwana wa
Ahikamu mwana wa Safani ndi lupanga, namupha iye, amene
mfumu ya ku Babulo inamuika wolamulira dziko. 3Ismayeli
naphanso Ayuda onse okhala naye Gedaliya pa Mizipa, ndi Akasidi
amene anakomana nao komweko, amuna a nkhondo. 4Ndipo
panali atapita masiku awiri atamupha Gedaliya, anthu
osadziwa, 5anadza anthu ocokera ku Sekemu, ndi ku Silo, ndi ku
Samariya, anthu makumi asanu ndi atatu, atameta ndebvu zao,
atang'amba zobvala zao, atadzitematema, ana tenga nsembe
zaufa ndi zonunkhira m'manja mwao, kunka nazo ku nyumba ya
Yehova. 6Ndipo Ismayeli mwana wa Netaniya anaturuka m'Mizipa
kukakomana nao, alinkuyenda ndi kulira misozi; ndipo panali,
pamene anakomana nao, anati kwa iwo, Idzani kwa Gedaliya
mwana wace wa Ahikamu. 7Ndipo panali, pamene analowa pakati
pa mudzi, Ismayeli mwana, wa Netaniya anawapha, nawaponya
pakati pa dzenje, iye ndi anthu okhala naye. 8Koma mwa iwo
anaoneka anthu khumi amene anati kwa Ismayeli, Musatiphe ife;
pakuti tiri ndi cuma cobisika m'mudzi, ca tirigu, ndi ca barele, ndi
ca mafuta, ndi ca uci. Momwemo analeka, osawapha pakati pa
abale ao. 9Ndipo dzenje moponyamo Ismayeli mitembo yonse ya
anthu amene anawapha, cifukwa ca Gedaliya, ndilo analipanga
mfumu Asa cifukwa ca kuopa Raasa mfumu ya Israyeli, lomwelo
Ismayeli mwana wa Netaniya analidzaza ndi ophedwawo. 10Ndipo
Ismayeli anatenga ndende otsala onse a anthu okhala m'Mizipa,
ana akazi a mfumu, ndi-anthu onse amene anatsala m'Mizipa,
amene Nebuzaradani kapitao wa alonda anapatsira Gedaliya
mwana wa Ahikamu; Ismayeli mwana wa Netaniya anawatenga
ndende, napita kukaolokera kwa ana a Amoni.
11Koma pamene Yohanani mwana wa Kareya, ndi akazembe Onse
a nkhondo akhala naye, anamva zoipa zonse anazicita Ismayeli
mwana wa Netaniya, 12anatenga anthu onse, nanka kukamenyana
ndi Ismayeli mwana wa Netaniya, nampeza pa madzi ambiri a
m'Gibeoni. 13Ndipo panali pamene anthu onse amene anali ndi
Ismayeli anaona Yohanani mwana wa Kareya, ndi akazembe onse a
nkhondo okhala naye, anasekera. 14Ndipo anthu onse amene
Ismayeli anatenga ndende kuwacotsa m'Mizipa anatembenuka
nabwera, nanka kwa Yohanani mwana wace wa Kareya, 15Koma

Ismayeli mwana wace wa Netaniya anapulumuka Yohanani ndi
anthu asanu ndi atatu, nanka kwa ana a Amoni. 16Ndipo Yohanani
mwana wace wa Kareya ndi akazembe onse a makamu amene
anali naye, anatenga anthu onse otsala a ku Mizipa, amene
anawabweza kwa Ismayeli mwana wace wa Netaniya atapha
Gedaliya mwana wace wa Ahikamu, anthu a nkhondo, ndi akazi,
ndi ana, ndi adindo, amene anawabwezanso ku Gibeoni; 17ndipo
anacoka, natsotsa m'Geruti-Kimamu, amene ali ku Betelehemu,
kunka kulowa m'Aigupto, 18cifukwa ca Akasidi; pakuti anawaopa,
cifukwa Ismayeli mwana wace wa Netaniya anapha Gedaliya
mwana wace wa Akikamu, amene mfumu ya ku Babulo anamuika
wolamulira m'dzikomo.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Yeremiya acenjeza anthu asapite ku Aigupto

1Ndipo akazembe onse a nkhondo, ndi Yohanani mwana wace wa
Kareya, ndi Jezaniya mwana wace wa Hosiya, ndi anthu onse
kuyambira wamng'ono, kufikira wamkuru, anayandikira, 2nati kwa
Yeremiya mneneri, Cipembedzero cathu cigwe pamaso panu,
nimutipempherere ife kwa Ambuye Mulungu wanu, cifukwa ca
otsala onsewa; pakuti tatsala ife owerengeka m'malo mwa ambiri,
monga maso anu ationa ife; 3kuti Yehova Mulungu wanu
atisonyeze ife njira imene tiyendemo, ndi comwe ticite. 4Ndipo
Yeremiya mneneri anati kwa iwo, Ndamva; taonani,
ndidzapemphera kwa Yehova Mulungu wanu monga mwa mau anu;
ndipo padzakhala kuti ciri conse Yehova adzakuyankhirani,
ndidzakufotokozerani; sindidzakubisirani inu kanthu. 5Pamenepo
iwo anati kwa Yeremiya, Yehova akhale mboni yoona ndi
yokhulupirika pakati pa ife, ngati siticita monga mwa mau onse
Yehova Mulungu wanu adzakutumizani nao kwa ife. 6Ngakhale ali
abwino, ngakhale ali oipa, ife tidzamvera mau a Yehova Mulungu
wathu, kwa Iye amene tikutumizani inu; kuti kutikomere, pomvera
mau a Yehova Mulungu wathu.
7Ndipo panali atapita masiku khumi, mau a Yehova anadza kwa
Yeremiya. 8Ndipo anaitana Yohanani mwana wace wa Kareya, ndi
akazembe onse a nkhondo okhala naye, ndi anthu onse kuyambira
wamng'ono kufikira wamkuru, 9nati kwa iwo, Atero Yehova,
Mulungu wa Israyeli, kwa Iye amene munandituma ine ndigwetse
pembedzero lanu pamaso pace, 10Ngati mudzakhalabe m'dziko
muno, ndidzamangitsa mudzi wanu, osakugumulani,
ndidzakuokani inu, osakuzulani; pakuti ndagwidwa naco cisoni
coipa cimene ndakucitirani inu. 11Musaope mfumu ya ku Babulo,
amene mumuopa; musamuope, ati Yehova: pakuti Ine ndiri ndi inu
kukupulumutsani, ndi kukulanditsani m'dzanja lace. 12Ndipo
ndidzakucitirani inu cifundo, li kuti iye akucitireni inu cifundo,
nakubwezereni inu ku dziko lanu. 13Koma mukati, Sitidzakhala
m'dziko muno; osamvera mau a Yehova Mulungu wanu; 14ndi kuti,
Iai; tidzanka ku Aigupto, kumene sitidzaona nkhondo, sitidzamva
kulira kwa lipenga, sitidzamva njala yokhumba mkate; pamenepo
tidzakhala; 15cifukwa cace mumve mau a Yehova, Otsala inu a
Yuda, atero Yehova wa makamu, Mulungu wa Israyeli, Ngati
mulozetsa nkhope zanu kuti mulowe m'Aigupto, kukakhala
m'menemo; 16pamenepo padzakhala, kuti lupanga limene muopa
lidzakupezani m'menemo m'dziko la Aigupto, ndi njala, imene
muiopa, idzakuumirirani kumeneko ku Aigupto; pamenepo
mudzafa. 17Kudzatero ndi anthu onse akulozetsa nkhope zao anke
ku Aigupto kuti akhale kumeneko; adzafa ndi lupanga, ndi njala,

ndi caola; ndipo wa iwo sadzatsala kapena kupulumuka ku coipa cimene ndidzatengera pa iwo ngakhale mmodzi yense. 18Pakuti atero Yehova wa makamu, Mulungu wa Israyeli: Monga mkwiyo wanga ndi ukali wanga wathiridwa kwa okhala m'Yerusalemu, momwemo ukali wanga udzathiridwa pa inu, pamene mudzalowa m'Aigupto; ndipo mudzakhala citukwano, ndi cizizwitso, ndi citemberero, ndi citonzo; ndipo simudzaonanso malo ano. 19Yehova wanena za inu, otsala inu a Yuda, Musalowe m'Aigupto; mudziwetu kuti ndakulangizani inu lero. 20Pakuti mwanyenga m'miyoyo yanu; pakuti mwandituma ine kwa Yehova Mulungu wanu, ndi kuti, Mutipempherere ife kwa Yehova Mulungu wathu; ndipo monga mwa zonse Yehova Mulungu wathu adzanena, momwemo mutifotokozere ife; ndipo tidzacita. 21Ndipo lero ndakufotokozerani, ndipo simunamva mau a Yehova Mulungu wanu m'cinthu ciri conse cimene Iye wanditumira ine naco kwa inu. 22Tsopano mudziwetu kuti mudzafa ndi lupanga, ndi njala ndi caola, komwe mufuna kukakhalako.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Amtenga Yeremiya napita naye ku Aigupto

1Ndipo panali pamene Yeremiya anatha kunena kwa anthu onse
mau onse a Yehova Mulungu wao, amene anamtuma iye nao
Yehova Mulungu wao, mau onse amenewo, 2pamenepo ananena
Azariya mwana wace wa Hosaya, ndi Yohanani mwana wace wa
Kareya, ndi anthu onse odzikuza, nati kwa Yeremiya, Unena
zonama; Yehova Mulungu wathu sanakutumiza iwe kudzanena,
Musalowe m'Aigupto kukhala m'menemo; 3koma Baruki mwana
wace wa Neriya aticicizira inu, mutipereke m'dzanja la Akasidi, kuti
atiphe ife, atitengere ife am'nsinga ku Babulo. 4Ndipo Yohanani
mwana wace wa Kareya, ndi akazembe onse a nkhondo, ndi anthu
onse sanamvera mau a Yehova, kuti akhale m'dziko la Yuda. 5Koma
Yohanani mwana wace wa Kareya, ndi akazembe onse: a nkhondo,
anatenga otsala onse a Yuda, amene anabwera ku mitundu yonse
kumene anaingitsidwirako kuti akhale m'dziko la Yuda; 6ndi amuna,
ndi akazi, ndi ana, ndi ana akazi a mfumu, ndi anthu onse amene
Nebuzaradani kapitao Wa alonda anasiya ndi Gedaliya mwana
wace wa Ahikamu, mwana wace wa Safani, ndi Yeremiya mneneri,
ndi Baruki mwana wace wa Neriya; 7ndipo anadza nalowa m'dziko
la Aigupto; pakuti sanamvera mau a Yehova; ndipo anadza mpaka
ku Tapanesi.

Yeremiya aneneratu kuti Nebukadirezara adzagonjetsa Aigupto

8Ndipo anafika mau a Yehova kwa Yeremiya m'Tapanesi,
kuti, 9Tenga miyala yaikuru m'dzanja lako, nuiyale ndi dothi pakati
pa njerwa, za pa khomo la nyumba ya Farao m'Tapanesi pamaso
pa anthu a Yuda; 10ndi kuti kwa iwo, Atero Yehova wa makamu,
Mulungu wa Israyeli: Taonani Ine ndidzatuma ndidzatenga
Nebukadirezara mfumu ya ku Babulo, mtumiki wanga, ndi kuika
mpando wace wacifumu pa miyalayi ndaiyala; ndipo iye
adzaibvundikira ndi hema wacifumu wace. 11Ndipo iye adzafika,
nadzakantha dziko la Aigupto; nadzapereka kuimfa iwo a kuimfa,
ndi kundende iwo a kundende, ndi kulupanga iwo a
kulupanga. 12Ndidzayatsa moto m'nyumba za milungu ya Aigupto;
ndipo adzazitentha, nadzaitenga ndende; ndipo adzadzipfunda ndi
dziko la Aigupto, monga mbusa abvala cobvala cace; nadzaturuka
m'menemo ndi mtendere. 13Ndipo adzatyola mizati ya zoimiritsa
za kacisi wa dzuwa, ali m'dziko la Aigupto; ndi nyumba za milungu
ya Aigupto adzazitentha ndi moto.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Yeremiya 44

Acenjeza mowaopsa Ayuda amene adathawira ku Aigupto

1Mau amene anadza kwa Yeremiya onena za Ayuda onse amene anakhala
m'dziko la Aigupto, okhala pa Migidoli, ndi pa Tapanesi, ndi pa Nofi, ndi
m'dziko la Patirosi, akuti, 2Atero Yehova wa makamu, Mulungu wa Israyeli:
Mwaona coipa conse cimene ndatengera pa Yerusalemu, ndi pa midzi yonse
ya Yuda; ndipo, taonani, lero lomwe iri bwinja, palibe munthu
wokhalamo; 3cifukwa ca coipa cao anacicita kuutsa naco mkwiyo wanga;
pakuti anapita kukafukizira, ndi kutumikira milungu yina, Imene sanaidziwa,
ngakhale iwo, ngakhale inu, ngakhale makolo anu. 4Koma ndinatuma kwa inu
atumiki anga onse aneneri, ndinauka mamawa ndi kuwatuma, ndi kuti,
Musacitetu conyansa ici ndidana naco. 5Koma sanamvera, sanachera khutu
lao kuti atembenuke asiye coipa cao, osafukizira milungu yina. 6Cifukwa cace
mkwiyo wanga ndi ukali wanga unathiridwa, nuyaka m'midzi ya Yuda ndi
m'miseu ya Yerusalemu; ndipo yapasudwa nikhala bwinja, monga lero
lomwe. 7Ndipo tsopano atero Yehova, Mulungu wa makamu, Mulungu wa
Israyeli: Cifukwa canji mucitira miyoyo yanu coipa ici, kudzisadzira nokha
amuna ndi akazi, makanda ndi oyamwa, pakati pa Yuda, osakusiyirani mmodzi
yense; 8popeza muutsa mkwiyo wanga ndi nchito ya manja anu, pofukizira
milungu yina m'dziko la Aigupto, kumene mwapita kukhalako; kuti mudulidwe,
ndi kuti mukhale citemberero ndi citonzo mwa amitundu onse a dziko
lapansi? 9Kodi mwaiwala zoipa za makolo anu, ndi zoipa za mafumu a Yuda,
ndi zoipa za akazi ao, ndi zoipa zanu, ndi za akazi anu, zimene anazicita
m'dziko la Yuda, ndi m'miseu ya Yerusalemu? 10Sanadzicepetse mpaka lero
lomwe, sanaope, sanayende m'cilamulo canga, kapena m'malemba anga,
amene ndinaika pamaso panu ndi pa makolo anu. 11Cifukwa cace atero
Yehova wa makamu, Mulungu wa Israyeli: Taonani, ndidzayang'anitsa nkhope
yanga pa inu ndikucitireni inu coipa, ndidule Yuda lonse. 12Ndipo
ndidzatengaotsala a Yuda, amene analozetsa nkhope zao alowe m'dziko la
Aigupto akhale m'menemo, ndipo adzathedwa onse; m'dziko la Aigupto
adzagwa, adzathedwa ndi lupanga ndi njala; adzafa kuyambira wamng'ono
mpaka wamkuru, ndi lupanga ndi njala; ndipo adzakhala citukwano, ndi
cizizwitso, ndi citemberero, ndi citonzo. 13Ndipo ndidzalanga iwo okhala
m'dziko la Aigupto, monga ndinalanga Yerusalemu, ndi lupanga, ndi njala, ndi
caola; 14kuti otsala a Yuda, amene ananka ku dziko la Aigupto kukhala
m'menemo, asapulumuke asatsale ndi mmodzi yense, kuti abwere ku dziko la
Yuda, kumene afuna kubwera kuti akhale m'menemo; pakuti adzabwera koma
adzapulumuka ndiwo.
15Ndipo amuna onse amene anadziwa kuti akazi ao anafukizira milungu yina,
ndi akazi onse omwe anaimirirapo, msonkhano waukuru, anthu onse okhala
m'dziko la Aigupto, m'Patirosi, anamyankha Yeremiya, kuti, 16Koma mau
amene wanena ndi ife m'dzina la Yehova, sitidzakumvera iwe. 17Koma
tidzacita ndithu mau onse anaturuka m'kamwa mwathu, kufukizira mfumu
yaikazi ya kumwamba, ndi kumthirira iye nsembe zothira, monga momwe
tikacitira ife, ndi atate athu, ndi mafumu athu ndi akuru athu, m'midzi ya
Yuda, ndi m'miseu ya Yerusalemu, pakuti pamenepo tinali ndi cakudya
cokwanira, tinakhala bwino, sitinaona coipa. 18Koma cilekere ife kufukizira
mfumu yaikazi ya kumwamba, ndi kumthirira iye nsembe zothira, tasowa
zonse, tathedwa ndi lupanga ndi caola. 19Ndipo pamene tinafukizira mfumu
yaikazi ya kumwamba, ndi kumthirira nsembe zothira, kodi tinamuumbira iye
mikate yakumpembedzera, ndi kumthirira nsembe zothira, opanda amuna

athu? 20Ndipo Yeremiya anati kwa anthu onse, kwa amuna, ndi kwa akazi,
kwa anthu onse amene anambwezera mau amenewa, ndi kuti, 21Zofukizira
zanu m'midzi ya Yuda, ndi m'miseu ya Yerusalemu, za inu ndi atate anu,
mafumu anu ndi akuru anu, ndi anthu a m'dziko, kodi Yehova
sanazikumbukira, kodi sizinalowa m'mtima mwace? 22ndipo Yehova sanatha
kupiririrabe, cifukwa ca macitidwe anu oipa, ndi cifukwa ca zonyansa zimene
munazicita; cifukwa cace dziko lanu likhala bwinja, ndi cizizwitso, ndi
citemberero, lopanda wokhalamo, monga lero lomwe. 23Cifukwa mwafukiza,
ndi cifukwa mwacimwira Yehova, osamvera mau a Yehova, osayenda
m'cilamulo cace, ndi m'malemba ace, ndi m'mboni zace, cifukwa cace coipaci
cakugwerani, monga lero lomwe.
24Ndiponso Yeremiya anati kwa anthu onse, ndi kwa akazi onse, Tamvani mau
a Yehova, nonse Ayuda amene muli m'dziko la Aigupto. 25Atero Yehova wa
makamu, Mulungu wa Israyeli, Inu ndi akazi anu mwanena ndi m'kamwa
mwanu, ndi kukwaniritsa ndi manja anu kuti, Tidzacita ndithu zowinda zathu
taziwindira, kufukizira mfumu yaikazi ya kumwamba, ndi kumthirira iye
nsembe zothira; khazikitsanitu zowinda zanu, citani zowinda zanu. 26Cifukwa
cace tamvani mau a Yehova, nonse Ayuda okhala m'dziko la Aigupto: Taonani,
ndalumbira, Pali dzina langa lalikuru, ati Yehova, kuti dzina langa
silidzachulidwanso m'kamwa mwa munthu ali yense wa Yuda m'dziko la
Aigupto, ndi kuti, Pali Yehova Mulungu. 27Taonani, ndiwayang'anira kuwacitira
zoipa, si zabwino; ndipo amuna onse a Yuda okhala m'dziko la Aigupto
adzathedwa ndi lupanga ndi njala, mpaka kutha kwao. 28Ndipo iwo amene
adzapulumuka kulupanga adzabwera kuturuka ku dziko la Aigupto kulowa
m'dziko la Yuda, owerengeka; ndipo otsala onse a Yuda, amene analowa
m'dziko la Aigupto kuti akhale m'menemo, adzadziwa ngati adzatsimikizidwa
mau a yani, kapena anga, kapena ao. 29Ndipo ici cidzakhala cizindikiro ca kwa
inu, ati Yehova, cakuti Ine ndidzakulangani m'malo muno, kuti mudziwe kuti
mau anga adzatsimikizidwatu akucitireni inu zoipa. 30Yehova atero: Taonani,
ndidzapereka Farao Hofra mfumu ya Aigupto m'manja a adani ace, ndi
m'manja a iwo akufuna moyo wace; monga ndinapereka Zedekiya mfumu ya
Yuda m'manja a Nebukadirezara mfumu ya ku Babulo mdani wace, amene
anafuna moyo wace.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Mau a Mulungu kwa Baruki

1Mau amene ananena Yeremiya mneneri kwa Baruki mwana wace
wa Neriya, pamene analemba mau awa m'buku ponena Yeremiya,
caka cacinai ca Yehoyakimu mwana wace wa Yosiya, mfumu ya
Yuda, ndi kuti, 2Yehova Mulungu wa Israyeli atero kwa inu,
Baruki: 3Munati, Kalanga ine tsopano! pakuti Yehova waonjezera
cisoni pa zowawa zanga; ndalema ndi kubuula kwanga, sindipeza
kupuma, 4Uzitero naye, Yehova atero: Taonani, cimene ndamanga
ndidzapasula, ndi cimene ndaoka ndidzazula; ndidzatero m'dziko
lonseli. 5Kodi udzifunira wekha zinthu zazikuru? usazifune; pakuti,
taona, ndidzatengera zoipa pa anthu onse, ati Yehova: koma moyo
wako ndidzakupatsa iwe ngati cofunkha m'malo monse m'mene
mupitamo.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Aneneratu kuti mfumu ya ku Babulo idzagonjetsa Aaigupto

1 Mau a Yehova amene anadza kwa Yeremiya mneneri akunena za
amitundu.
2 Za Aigupto: kunena za nkhondo ya Farao-neko mfumu ya Aigupto,
imene inali pa nyanja ya Firate m'Karikemisi, imene anaikantha
Nebukadirezara mfumu ya ku Babulo caka cacinai ca Yehoyakimu
mwana wace wa Yosiya, mfumu ya Yuda.
3 Konzani cikopa ndi lihawo, nimuyandikire kunkhondo. 4 Mangani
akavalo, bwerani, inu apakavalo, imani ndi zisoti zacitsulo; tuulani
nthungo zanu, bvalani malaya acitsulo. 5 Cifukwa canji ndaciona?
aopa, abwerera; amphamvu ao agwetsedwa, athawadi, osaceukira
m'mbuyo; mantha ali ponseponse, ati Yehova. 6 Waliwiro asathawe,
wamphamvu asapulumuke; kumpoto pambali pa nyanja ya Firate
wapunthwa nagwa. 7 Ndani uyu amene auka ngati Nile, madzi ace
ogabvira monga nyanja? 8 Aigupto auka ngati Nile, madzi ace
agabvira ngati nyanja; ndipo ati, Ndidzauka, ndidzamiza dziko
lapansi; ndidzaononga mudzi ndi okhalamo ace. 9 Kwerani, inu
akavalo; citani misala, inu magareta, aturuke amphamvu; Akusi ndi
Aputi, ogwira cikopa; ndi Aludi, amene agwira ndi kukoka
uta. 10 Pakuti tsikulo ndi la Ambuye, Yehova wa makamu, tsiku
lakubweza cilango, kuti abwezere cilango adani ace; ndipo lupanga
lidzadya, lidzakhuta, nilidzamwetsa mwazi wao; pakuti Ambuye,
Yehova wa makamu, ali ndi nsembe m'dziko la kumpoto pa nyanja
ya Firate. 11 Kwera ku Gileadi, tenga bvunguti, namwali iwe mwana
wa Aigupto; wacurukitsa mankhwala cabe; palibe kucira
kwako. 12 Amitundu amva manyazi anu, dziko lapansi ladzala ndi
kupfuula kwanu; pakuti amphamvu akhumudwitsana, agwa onse
awiri pamodzi.
13 Mau amene Yehova ananena kwa Yeremiya mneneri, kuti
Nebukadirezara mfumu ya ku Babulo adzafika adzakantha dziko la
Aigupto.
14 Nenani m'Aigupto, lalikirani m'Migidoli, lalikirani m'Nofi ndi
Tapanesi; nimuti, Udziimike, nudzikonzere wekha; pakuti lupanga
ladya pozungulira pako. 15 Akulimba ako akokoledwa bwanji?
sanaime, cifukwa Yehova anawathamangitsa, 16 Anapunthwitsa
ambiri, inde, anagwa wina pa mnzace, ndipo anati, Ukani, tinkenso
kwa anthu athu, ku dziko la kubadwa kwathu, kucokera ku lupanga
lobvutitsa. 17 Ndipo anapfuula kumeneko, Farao mfumu ya Aigupto
ndiye phokoso lokha; wapititsa nthawi yopangira, 18 Pali Ine, ati
Mfumu, dzina lace ndi Yehova wa makamu, ndithu monga Tabori
mwa mapiri, monga Karimeli pambali pa nyanja, momwemo
adzafika. 19 Mwana wamkazi iwe wokhala m'Aigupto, dzikonzere
kunka kundende; pakuti Nofi adzakhala bwinja, nadzapsya,

mulibenso wokhalamo. 20Aigupto ndi ng'ombe ya msoti yosalala;
cionongeko cituruka kumpoto cafika, cafika. 21Ndiponso olipidwa
ace ali pakati pace onga ngati ana a ng'ombe a m'khola; pakuti
iwonso abwerera, athawa pamodzi, sanaime; pakuti tsiku la tsoka
lao linawafikira, ndi nthawi ya kuweruzidwa kwao. 22Mkokomo
wace udzanga wa njoka yothawa; pakuti adzayenda ndi nkhondo,
adzafika kumenyana naye ndi nkhwangwa, monga akutema
mitengo. 23Adzatema nkhalango yace, ati Yehova, pokhala
yosapitika; pakuti acuruka koposa dzombe, ali
osawerengeka. 24Mwana wace wamkazi wa Aigupto adzacitidwa
manyazi, adzaperekedwa m'manja a anthu a kumpoto. 25Yehova
wa makamu, Mulungu wa Israyeli, ati: Taonani, ndidzalanga Amoni
wa No, ndi Farao, ndi Aigupto, pamodzi ndi milungu yace, ndi
mafumu ace; ngakhale Farao, ndi iwo akumkhulupirira iye; 26ndipo
ndidzawapereka m'manja a iwo amene afuna moyo wao, ndi
m'dzanja la Nebukadirezara mfumu ya ku Babulo, ndi m'manja a
atumiki ace; pambuyo pace adzakhalamo anthu, monga masiku
akale, ati Yehova. 27Koma usaope iwe, mtumiki wanga Yakobo,
usacite mantha, iwe Israyeli: pakuti, taona, ndidzakupulumutsa iwe
kucokera kutari, ndi mbeu yako ku dziko la undende wao, ndipo
Yakobo adzabwera, nadzapumula m'mtendere, ndipo palibe amene
adzamuopetsa iye, 28Usaope, iwe Yakobo mtumiki wanga, ati
Yehova; pakuti Ine ndiri ndi iwe; pakuti Ine ndidzathetsa mitundu
yonse kumene ndinakuingitsirako iwe, koma sindidzakuthetsa iwe;
koma ndidzakulangiza ndi ciweruziro, ndipo sindidzakusiya konse
wosalangidwa.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Aneneratu za citsutso ca Afilisti

1 Mau a Yehova amene anadza kwa Yeremiya mneneri onena za
Afilisti, Farao asanakanthe Gaza.
2 Yehova atero: Taonani, madzi adzakwera kuturuka kumpoto,
nadzakhala mtsinje wosefuka, nadzasefukira padziko ndi pa zonse
ziri m'mwemo, pamudzi ndi pa onse okhalamo; ndipo amuna
adzalira, ndi onse okhala m'dziko adzakuwa. 3 Pomveka migugu ya
ziboda za olimba ane, pogumukira magareta ace, ndi pophokosera
njinga zace, atate sadzaceukira ana ao cifukwa ca kulefuka kwa
manja ao; 4 cifukwa ca tsiku lakudzafunkha Afilisti onse, kuphera
Turo ndi Zidoni othangata onse akutsala; pakuti Yehova adzafunkha
Afilisti, otsala a cisumbu ca Kafitori. 5 Dazi lafikira a Gaza; Asikeloni
wathedwa, otsala m'cidikha cao; udzadziceka masiku angati? 6 Iwe
lupanga la Yehova, atsala masiku angati osakhala cete iwe?
dzilonge wekha m'banzi lako; puma, nukhale cete. 7 Udzakhala cete
bwanji, popeza Yehova anakulangiza? za Asikeloni, ndi za m'mbali
mwa nyanja, pamenepo analiika.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Citsutso ca Moabu

1Za Moabu Atero Yehova wa makamu, Mulungu wa Israyeli: Tsoka
Nebo! pakuti wapasuka; Kiriyataimu wacitidwa manyazi,
wagwidwa; linga la pamtunda lacitidwa manyazi
lapasudwa. 2Palibenso kutamanda Moabu; m'Hesiboni
anamlingiririra zoipa, ndi kuti, Tiyeni, tiwathe asakhalenso mtundu
waanthu. Iwenso, Madimeni, udzatontholetsedwa, lupanga
lidzakulondola iwe. 3Mau amveka kucokera ku Horonaimu,
kufunkha ndi kuononga kwakukuru! 4Moabu waonongedwa;
ang'ono ace amveketsa kulira. 5Pakuti adzakwera pa cikweza ca
Luhiti ndi kulira kosaleka; pakuti pa citsiko ca Horonaimu amva
kulira kowawa kwa cionongeko. 6Thawani, pulumutsani miyoyo
yanu, mukhale amarisece m'cipululu, 7Pakuti, cifukwa
wakhulupirira nchito zanu ndi cuma canu, iwenso udzagwidwa;
ndipo Kemosi adza kundende, ansembe ace ndi akuru ace
pamodzi. 8Ndipo wakufunkha adzafikira pa midzi yonse,
sudzapulumuka mudzi uli wonse; cigwa comwe cidzasakazidwa,
ndipo cidikha cidzaonongedwa; monga wanena Yehova. 9Patsani
Moabu mapiko, kuti athawe apulumuke; midzi yace ikhale bwinja,
lopanda wokhalamo. 10Atembereredwe iye amene agwira nchito ya
Yehova monyenga, atembereredwe iye amene abweza lupanga
lace kumwazi. 11Moabu wakhala m'mtendere kuyambira ubwana
wace, wakhala pansenga, osatetekulidwa, sananke kundende;
cifukwa cace makoleredwe ace alimobe mwa iye, pfungo lace
silinasinthika. 12Cifukwa cace, taonani, masiku adza, ati Yehova,
amene ndidzatuma kwa iye otsanula, amene adzamtsanula iye;
adzataya za mbiya zace, nadzaswa zipanda zao. 13Ndipo Moabu
adzacita manyazi cifukwa ca Kemosi, monga nyumba ya Israyeli
inacita manyazi cifukwa ca Beteli amene anamkhulupirira, 14Muti
bwanji, Tiri amphamvu, olimba mtima ankhondo? 15Moabu
wapasuka, akwera kulowa m'midzi yace, ndi anyamata ace
osankhika atsikira kukaphedwa, ati Mfumu, dzina lace ndiye
Yehova wa makamu. 16Tsoka la Moabu layandikira kudza, nsautso
yace ifulumiratu. 17Inu nonse akumzungulira, mumcitire iye cisoni,
inu nonse akudziwa dzina lace; muti, Cibonga colimba catyokatu,
ndodo yokoma! 18Iwe mwana wamkazi wokhala m'Diboni, utsike
pa ulemerero wako, nukhale ndi ludzu; pakuti wakufunkha Moabu
wakukwerera, iwe waononga malinga ako. 19Iwe wokhala m'Aroeri,
ima panjira, nusuzumire umfunse iye amene athawa, ndi mkazi
amene apulumuka; nuti, Cacitidwa ciani? 20Moabu wacitidwa
manyazi, pakuti watyoka; kuwa nulire, nunene m'Arinoni, kuti
Moabu wapasuka. 21Ciweruzo cafika pa dziko lacidikha; pa Holoni,
ndi pa Yaza, ndi pa Mefati; 22ndi pa Diboni, ndi pa Nebo, ndi pa

Beti-Dibilataimu; 23ndi pa Kiriataimu, ndi pa Beti-Gamuli, ndi pa
Beti-Meoni; 24ndi pa Kerioti, ndi pa Bozira, ndi pa midzi yonse ya
dziko la Moabu, yakutari kapena yakufupi. 25Nyanga ya Moabu
yaduka, ndipo watyoka mkono wace, ati Yehova. 26Umledzeretse
iye; pakuti anadzikuza pokana Yehova; Moabu yemwe
adzabvimvinika m'kusanza kwace, ndipo iye
adzasekedwanso. 27Kodi sunaseka Israyeli? Kodi iye anapezedwa
mwa mbala? pakuti nthawi zonse unena za iye, upukusa
mutu. 28Inu okhala m'Moabu, siyani midzi, khalani m'thanthwe;
nimukhale monga njiwa imene isanja cisanja cace pambali
pakamwa pa dzenje. 29Ife tamva kudzikuza kwa Moabu, wadzikuza
ndithu, kunyang'wa kwace, ndi kunyada kwace, ndi kudzitama
kwace, ndi kudzikuza kwa mtima wace.
30Ine ndidziwa mkwiyo wace, ati Yehova, kuti uli cabe; zonyenga
zace sizinacita kanthu. 31Cifukwa cace ndidzakuwira Moabu; inde,
ndidzapfuulira Moabu yense, adzalirira anthu a ku Kirere. 32Iwe
mpesa wa Sibima; ndidzakulirira iwe ndi kulira kopambana kulira
kwa Yazeri, nthambi zako zinapitirira nyanja, zinafikira ku nyanja
ya Yazeri; wakufunkha wagwera zipatso zako za mpakasa ndi
mphesa zako. 33Ndipo kusekera ndi kukondwa kwacotsedwa, ku
munda wobala ndi ku dziko la Moabu; ndipo ndaletsa vinyo pa
zoponderamo; sadzaponda ndi kupfuula; kupfuula sikudzakhala
kupfuula. 34Kuyambira kupfuula kwa Hesiboni mpaka ku Eleale,
mpaka ku Yahazi anakweza mau, kuyambira pa Zoari mpaka ku
Horonaimu, ku Egilati-Selisiya; pakuti pa madzi a ku Nimurimu
komwe padzakhala mabwinja. 35Ndiponso ndidzaletsa m'Moabu,
ati Yehova, iye amene apereka nsembe pamsanje, ndi iye amene
afukizira milungu yace. 36Cifukwa cace mtima wanga umlima
Moabu monga zitolilo, ndipo mtima wanga uwalirira anthu a
Kireresi monga zitolilo, cifukwa cace zakucuruka zace adadzionera
zatayika. 37Pakuti mitu yonse iri yadazi, ndipo ndebvu ziri
zosengedwa; pa manja onse pali pocekedwa-cekedwa, ndi
pacuuno ciguduli. 38Pamwamba pa macindwi a Moabu ndi m'miseu
mwace muli kulira monse monse; pakuti ndaswa Moabu monga
mbiya m'mene mulibe cikondwero, ati Yehova. 39Yasweka bwanji!
Akuwa bwanji Moabu! Wapotoloka bwanji ndi manyazi! Comweco
Moabu adzakhala coseketsa ndi coopsera onse omzungulira
iye. 40Pakuti Yehova atero: Taonani, adzauluka ngati
ciombankhanga, adzamtambasulira Moabu mapiko ace. 41Keroti
walandidwa, ndi malinga agwidwa, ndipo tsiku lomwelo mtima wa
anthu amphamvu a Moabu adzakhala ngati mtima wa mkazi
alinkudwala. 42Ndipo Moabu adzaonongeka asakhalenso mtundu
wa anthu, cifukwa anadzikuzira yekha pa Yehova. 43Mantha, ndi
dzenje, ndi khwekhwe, ziri pa iwe, wokhala m'Moabu, ati

Yehova. 44Ndipo iye wakuthawa cifukwa ca mantha adzagwa
m'dzenje; ndi iye amene aturuka m'dzenje adzagwidwa
m'khwekhwe; pakuti ndidzatengera pa iye, pa Moabu, caka ca
kulangidwa kwao, ati Yehova. 45Iwo amene anathawa aima opanda
mphamvu pansi pa mthunzi wa Hesiboni; pakuti moto waturuka
m'Hesiboni, ndi malawi a moto m'kati mwa Sihoni, nadya ngondya
ya Moabu, ndi pakati pamtu pa ana a phokoso, 46Tsoka iwe,
Moabu! anthu a Kemosi athedwa; pakuti ana ako amuna
atengedwa ndende, ndi ana ako akazi atengedwa ndende. 47Koma
ndidzabwezanso undende wa Moabu masiku akumariza, ati
Yehova. Ziweruzo za Moabu ndi zomwezi.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Citsutso ca Aamoni

1Za ana a Amoni. Yehova atero: Kodi Israyeli alibe ana amuna?
alibe wolowa dzina? M'mwemo mfumu yao yalowa pa Gadi cifukwa
canji, ndi anthu ace akhala m'midzi mwace? 2Cifukwa cace,
taonani, masiku afika, ati Yehova, Ine ndidzamveketsa mpfuu ya
nkhondo yomenyana ndi Raba wa ana a Amoni; ndipo
adzasanduka muunda wabwinja, ndipo ana ace akazi
adzatenthedwa ndi moto; pamenepo Israyeli adzalanda iwo amene
adamlanda, ati Yehova. 3Kuwa, iwe Hesiboni, pakuti Ai wapasuka;
lirani, inu ana akazi a Raba, mubvale ciguduli; citani maliro,
thamangani kwina ndi kwina pamipanda; pakuti mfumu yao
idzalowa m'ndende, ansembe ace ndi akuru ace pamodzi. 4Cifukwa
canji udzitamandira ndi zigwa, cigwa cako coyendamo madzi, iwe
mwana wamkazi wobwerera m'mbuyo, amene anakhulupirira
cuma cace, nati, Adza kwa ine ndani? 5Taona ndidzakutengera
mantha, ati Ambuye, Yehova wa makamu, akucokera kwa onse
amene akuzungulira iwe; ndipo mudzaingitsidwa yense kulozera
maso ace, ndipo palibe amene adzasonkhanitsa osocera. 6Koma
pambuyo pace ndidzabwezanso undende wa ana a Amoni, ati
Yehova.

Za kulangidwa kwa Aedomu

7Za Edomu. Yehova wa makamu atero: Kodi m'Temani mulibenso
nzeru? kodi uphungu wawathera akucenjera? kodi nzeru zao zatha
psiti? 8Thawani inu, bwerani, khalani mwakuya, inu okhala
m'Dedani; pakuti ndidzatengera pa iye tsoka la Esau, nthawi yoti
ndidzamlanga iye. 9Akafika kwa inu akuchera mphesa, sadzasiya
mphesa zokunkha? akafika usiku akuba, adzaononga mpaka
kutha? 10Pakuti ndambvula Esau, ndambvundukula, sadzatha
kubisala; mbeu zace zaonongeka, ndi abale ace, ndi anansi ace,
ndipo palibe iye. 11Siya ana ako amasiye, Ine ndidzawasunga;
akazi ako amasiye andikhulupirire Ine. 12Pakuti Yehova atero:
Taonani, iwo amene sanaweruzidwa kuti amwe cikho adzamwadi;
kodi iwe ndiye amene adzakhala wosalangidwa konse? sudzakhala
wosalangidwa, koma udzamwadi. 13Pakuti ndalumbira, Pali Ine, ati
Yehova, kuti Boma adzakhala cizizwitso, citonzo, copasuka, ndi
citemberero; ndipo midzi yace yonse idzakhala yopasuka
cipasukire. 14Ndamva mthenga wa kwa Yehoya, ndipo mthenga
watumidwa mwa amitundu, wakuti, Sonkhanani, mumdzere,
nimuukire nkhondo. 15Pakuti, caona, ndakuyesa iwe wamng'ono
mwa amitundu, ndi wonyozedwa mwa anthu. 16Koma za kuopsya
kwako, kunyada kwa mtima wako kunakunyenga iwe, wokhala
m'mapanga a thanthwe, woumirira msanje wa citunda, ngakhale
usanja cisanja cako pamwamba penipeni ngati ciombankhanga,

ndidzakutsitsa iwe kumeneko, ati Yehova. 17Ndipo Edomu
adzakhala cizizwitso; ndipo yense wakupitapo adzazizwa, ndipo
adzatsonyera zobvuta zace zonse. 18Monga m'kupasuka kwa
Sodomu ndi Gomora ndi midzi inzace, ati Yehova, munthu ali yense
sadzakhala m'menemo, mwana wa munthu ali yense sadzagona
m'menemo. 19Taona, wina adzakwerera mudzi wolimba ngati
mkango wocokera ku Yordano wosefuka; koma dzidzidzi
ndidzamthamangitsa amcokere; ndipo ali yense amene
asankhidwa, ndidzamuika woyang'anira wace, pakuti wakunga Ine
ndani? adzandiikira nthawi ndani? ndipo mbusa adzaima pamaso
panga ndani? 20Cifukwa cace tamvani uphungu wa Yehova, umene
waupangira pa Edomu; ndi zimene walingalirira okhala m'Temani,
ndithu adzawakoka, ana ang'ono a zoweta; ndithu adzayesa busa
lao bwinja pamodzi nao. 21Dziko lapansi linthunthumira ndi
phokoso lja kugwa kwao; pali mpfuu, phokoso lace limveka pa
Nyanja Yofiira. 22Taonani, adzafika nadzauluka ngati
ciombankhanga, adzatambasulira Boma mapiko ace, ndipo tsiku
lomwelo mtima wa anthu amphamvu a Edomu adzakhala ngati
mtima wa mkazi alinkudwala.

Citsutso ca Damasiko

23Za Damasiko. Hamati ndi Aripadi ali ndi manyazi, cifukwa
anamva malodza, asungunuka kunyanja, adera nkhawa osatha
kukhala cete. 24Damasiko walefuka, atembenukira kuti athawe,
kunthunthumira kwamgwira; zobvuta ndi kulira zamgwira iye, ngati
mkazi alimkudwala. 25Alekeranji kusiya mudzi wa cilemekezo,
mudzi wa cikondwero canga? 26Cifukwa cace anyamata ace
adzagwa m'miseu yace, ndipo anthu onse a nkhondo
adzatontholetsedwa tsiku lomwelo, ati Yehova wa
makamu. 27Ndipo Ine ndidzayatsa moto m'khoma la Damasiko,
udzathetsa zinyumba za Beni-Hadadi.

Citsutso ca Kedara, Hazori ndi Elamu

28Za Kedara, ndi za maufumu a Hazori, amene anawakantha
Nebukadirezara mfumu ya ku Babulo.
Yehova atero: Ukani, kwerani ku Kedara, funkhani ana a
kum'mawa. 29Mahema ao ndi zoweta zao adzazilanda,
adzadzitengera nsaru zocingira zao, ndi katundu wao yense, ndi
ngamila zao; ndipo adzapfuulira iwo, Mantha ponse
ponse. 30Thawani inu, yendani kutari, khalani mwakuya, Inu okhala
m'Hazori, ati Yehova; pakuti Nebukadirezara mfumu ya ku Babulo
anapangira uphungu pa inu, nakulingalirirani. 31Nyamukani,
kwererani mtundu wokhala ndi mtendere, wokhala osadera
nkhawa, ati Yehova, amene alibe zitseko ndi mipiringidzo, okhala
pa okha. 32Ndipo ngamila zao zidzakhala zofunkha, ndi unyinji wa
ng'ombe zao udzakhala wolanda; ndipo ndidzabalalitsira ku

mphepo zonse iwo amene ameta m'mbali mwa tsitsi lao; ndipo
ndidzatenga tsoka lao ku mbali zao zonse, ati Yehova. 33Ndipo
Hazori adzakhala mokhalamo ankhandwe, bwinja lacikhalire;
simudzakhalamo munthu, simudzagonamo mwana wa munthu.
34Mau a Yehova amene anafika kwa Yeremiya mneneri, onena za
Elamu poyamba kulamulira Zedekiya mfumu ya Yuda,
kuti, 35Yehova wa makamu atero: Taonani, ndidzatyola uta wa
Elamu, ndiwo mtima wa mphamvu yao. 36Pa Elamu ndidzatengera
mphepo zinai ku mbali zinai za mlengalenga, ndidzamwaza iwo ku
mphepo zonsezo; ndipo sikudzakhala mtundu kumene
opitikitsidwa a Elamu sadzafikako. 37Ndipo ndidzacititsa Elamu
mantha pamaso pa amaliwongo ao, ndi pamaso pa iwo ofuna
moyo wao; ndipo ndidzatengera coipa pa iwo, mkwiyo wanga
waukali, ati Yehova; ndipo ndidzatumiza lupanga liwalondole,
mpaka nditawatha; 38ndipo ndidzaika mpando wacifumu wanga
m'Elamu, ndipo ndidzaononga pamenepo mfumu ndi akulu, ati
Yehova. 39Koma padzaoneka masiku akutsiriza, kuti
ndidzabwezanso undende wa Elamu, ati Yehova.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Citsutso ca Babulo

1Mau amene ananena Yehova za Babulo, za dziko la Akasidi, mwa
Yeremiya mneneri.
2Lalikirani mwa amitundu, falikitsani, kwezani mbendera;
falikitsani, musabise; munene, Babulo wagwidwa, Beli wacitidwa
manyazi, Merodake watyokatyoka, zosema zace zacitidwa
manyazi, mafano ace atyokatyoka. 3Pakuti mtundu wa anthu
udzaturuka kumpoto kudzamenyana naye, udzacititsa dziko lace
bwinja, losakhalamo anthu; athawa, apita, anthu ndi
nyama. 4Masiku omwewo, nthawi yomweyo, ati Yehova, ana a
Israyeliadzadza, iwo ndi ana a Yuda; pamodzi adzayenda m'njira
mwao alinkulira, nadzafuna Yehova Mulungu wao. 5Adzafunsira
Ziyoni nkhope zao zirikuyang'ana kumeneko, ndi kuti, Tiyeni inu,
dzilumikizeni kwa Yehova m'cipangano ca muyaya cimene
sicidzaiwalika.
6Anthu anga anakhala nkhosa zotayika; abusa ao anazisokeretsa
pa mapiri onyenga; acoka kuphiri kunka kucitunda; aiwala malo ao
akupuma. 7Onse amene anazipeza anazidya; adani ao anati,
Sitiparamula mlandu, cifukwa iwo anacimwira Yehova, ndiye
mokhalamo zolungama, Yehova, ciyembekezo ca atate
ao. 8Thawani pakati pa Babulo, turukani m'dziko la Akasidi,
mukhale monga atonde patsogolo pa zoweta. 9Pakuti, taonani,
ndidzabukitsa ndidzafikitsa kudzamenyana ndi Babulo msonkhano
wa mitundu yaikuru kucokera ku dziko la kumpoto; ndipo adzaguba
pomenyana ndi iye; kumeneko Babulo adzacotsedwa; mibvi yao
idzakhala ngati ya munthu wamaluli wamphamvu; yosabwera
cabe. 10Ndipo Kasidi adzakhala cofunkha; onse amene
amfunkhitsa iye adzakhuta, ati Yehova. 11Cifukwa mukondwa,
cifukwa musekerera, inu amene mulanda colowa canga, cifukwa
muli onenepa monga ng'ombe yamsoti yoponda tirigu, ndi kulira
ngati akavalo olimba; 12amai anu adzakhala ndi manyazi ambiri;
amene anakubalani adzathedwa nzeru; taonani, adzakhala
wapambuyo wa amitundu, cipululu, dziko louma, bwinja. 13Cifukwa
ca mkwiyo wa Yehova sadzakhalamo anthu, koma padzakhala
bwinja; onse akupita pa Babulo adzadabwa, adzatsonyera pa
zobvuta zace zonse. 14Gubani ndi kuzungulira Babulo kumenyana
naye, inu nonse okoka uta; mumponyere iye, osaderera mibvi;
pakuti wacimwira Yehova. 15Mumpfuulire iye pomzungulira iye;
pakuti wagwira mwendo; malinga ace agwa; makoma ace
agwetsedwa; pakuti ndi kubwezera cilango kwa Yehova;
mumbwezere cilango; monga iye wacita mumcitire iye
momwemo. 16Muwathe ofesa ku Babulo, ndi iwo amene agwira
zenga nyengo ya masika; cifukwa ca lupanga losautsa

adzatembenukira yense kwa anthu ace, nadzathawira yense ku dziko lace.
17Israyeli ndiye nkhosa yolowerera, mikango yampitikitsa, poyamba inamudya mfumu ya Asuri; ndipo pomariza Nebukadirezara uyo watyola mafupa ace. 18Cifukwa cace atero Yehova wa makamu, Mulungu wa Israyeli: Taonani, ndidzalanga mfumu ya ku Babulo ndi dziko lace, monga ndinalanga mfumu ya Asuri. 19Ndipo ndidzabwezeranso Israyeli ku busa lace, ndipo adzadya pa Karimeli ndi pa Basana, moyo wace nudzakhuta pa mapiri a Efraimu ndi m'Gileadi. 20Masiku omwewo, nthawi yomweyo, ati Yehova, zoipa za Israyeli zidzafunidwa, koma zidzasoweka; ndi zocimwa za Yuda, koma sizidzapezeka; pakuti ndidzakhululukira iwo amene ndidzawasiya ngati cotsala.
21Kwera kukamenyana ndi dziko la Merataimu, ndi okhala m'Pekoli, ipha nuononge konse pambuyo pao, ati Yehova, cita monga mwa zonse ndinakuuza iwe. 22Phokoso la nkhondo liri m'dziko lino, ndi lakuononga kwakukuru. 23Nyundo ya dziko lonse yaduka ndi kutyoka! Babulo wasandulca bwinja pakati pa amitundu! 24Ndakuchera iwe msampha, ndi iwenso wagwidwa, iwe Babulo, ndipo sunadziwa, wapezeka, ndiponso wagwidwa, cifukwa walimbana ndi Yehova. 25Yehova watsegula pa nyumba ya zida zace, ndipo waturutsa zida za mkwiyo wace; pakuti Ambuye Yehova wa makamu, ali ndi nchito m'dziko la Akasidi. 26Tadzani kudzamenyana ndi iye kucokera ku malekezero ace, tsegulani pa nkhokwe zace; unjikani zace monga miyulu, mumuononge konse; pasatsale kanthu ka pa iye. 27Iphani ng'ombe zamphongo zace zonse; zitsikire kukaphedwa; tsoka iwo! pakuti tsiku lao lafika, tsiku la kulanga kwao. 28Mau a iwo akuthawa akupulumuka m'dziko la Babulo, kuti alalikire m'Ziyoni kubwezera cilango kwa Yehova Mulungu wathu, kubwezera cilango cifukwa ca Kacisi wace. 29Memezani amauta amenyane ndi Babulo, onse amene akoka uta; mummangire iye zitando pomzungulira iye, asapulumuke mmodzi wace yense; mumbwezere iye monga mwa nchito yace; monga mwa zonse wazicita, mumcitire iye; pakuti anamnyadira Yehova, Woyera wa Israyeli. 30Cifukwa cace anyamata ace adzagwa m'miseu yace, ndi anthu ankhondo ace onse adzatontholetsedwa tsiku lomwelo, ati Yehova. 31Taonani, nditsutsana nawe, wonyada iwe, ati Ambuye, Yehova wa makamu; pakuti tsiku lako lafika, nthawi imene ndidzakulanga iwe. 32Ndipo wonyadayo adzakhumudwa nadzagwa, ndipo palibe amene adzamuutsa iye; ndipo Ine ndidzayatsa moto m'midzi yace, ndipo udzatentha onse akumzungulira iye.
33Yehova wa makamu atero: Ana a Israyeli ndi ana a Yuda asautsidwa pamodzi; ndipo onse amene anawagwira ndende

awagwiritsitsa; akana kuwamasula. 34Mombolo wao ngwa
mphamvu; dzina lace Yehova wa makamu: adzawanenera mlandu
wao ndithu; kuti apumitse dziko lapansi, nadzidzimutse okhala
m'Babulo. 35Lupanga liri pa Akasidi, ati Yehova, pa okhala
m'Babulo, pa akuru ace, ndi pa anzeru ace. 36Lupanga liri pa
amatukutuku, ndipo adzapusa; lupanga liri pa anthu olimba ace,
ndipo adzaopa. 37Lupanga liri pa akavalo ao, ndi pa magareta ao,
ndi pa anthu onse osanganizidwa amene ali pakati pace, ndipo
adzakhala ngati akazi; lupanga liri pa cuma cace, ndipo
cidzalandidwa. 38Cirala ciri pa madzi ace, ndipo adzaphwa; pakuti
ndi dziko la mafano osema, ndipo ayaruka ndi kufuna
zoopsa. 39Cifukwa cace zirombo za kucipululu ndi mimbulu
zidzakhalamo, ndi nthiwatiwa zidzakhala m'menemo; ndipo
sadzakhalamo anthu konse; ndipo sadzakhalamo m'mibadwo
mibadwo. 40Monga muja Yehova anagwetsa Sodomu ndi Gomora
ndi midzi Inzace, ati Yehova; anthu sadzakhalamo, mwana wa
munthu sadzagonamo. 41Taonani, anthu acokera kumpoto; ndiwo
mtundu waukuru, ndipo mafumu ambiri adzaukitsidwa kucokera ku
malekezero a dziko lapansi. 42Agwira uta ndi nthungo; ali
ankharwe, alibe cifundo; mau ao apokosera ngati nyanja, ndipo
akwera akavalo, yense aguba monga munthu wa kunkhondo,
kukamenyana ndi iwe, mwana wamkazi wa Babulo. 43Mfumu ya ku
Babulo yamva mbiri yao, ndipo manja ace alefuka; wagwidwa ndi
nkhawa, ndi zowawa zonga za mkazi alimkudwala. 44Taonani,
mtundu uja adzakwerera mudzi wolimba ngati mkango wocokera
ku Yordano wosefuka; koma dzidzidzi ndidzauthamangitsa
umcokere, ndipo ali yense amene asankhidwa, ndidzamuika
woyang'anira wace; pakuti wakunga Ine ndani? adzandiikira nthawi
ndani? ndipo mbusa adzaima pamaso panga ndani? 45Cifukwa
cace tamvani uphungu wa Yehova, umene waupangira pa Babulo;
ndi zimene walingirira dziko la Akasidi; ndithu adzawakoka, ana
ang'ono a zoweta; ndithu adzayesa busa lao bwinja pamodzi
nao. 46Dziko lapansi linthunthumira, pa phokoso la kugwidwa kwa
Babulo, ndipo mpfuu wamveka mwa amitundu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

1Yehova atero: Taonani, ndidzaukitsira Babulo, ndi iwo okhala
m'Lebi-kamai, mphepo yoononga, 2Ndipo ndidzatuma ku Babulo
alendo, amene adzamkupira iye, amene adzataya zonse m'dziko
lace, pakuti tsiku la cisauko adzamenyana ndi iye pomzungulira
pace. 3Wauta asakoke uta wace, asadzikweze m'malaya ace
acitsulo; musasiye anyamata ace; muononge ndithu khamu lace
lonse. 4Ndipo adzagwa ophedwa m'dziko la Akasidi, opyozedwa
m'miseu yace. 5Pakuti Israyeli ndi Yuda sasiyidwa ndi Mulungu wao,
ndiye Yehova wa makamu: ngakhale dziko lao ladzala ndi ucimo
kucimwira Woyera wa Israyeli. 6Thawani pakati pa Babulo, yense
apulumuke moyo wace; musathedwe m'coipa cace; pakuti ndi
nthawi ya kubwezera cilango; Yehova adzambwezera iye mphotho
yace. 7Babulo wakhala cikho cagolidi m'dzanja la Yehova, amene
analedzeretsa dziko lonse lapansi; amitundu amwa vinyo wace;
cifukwa cace amitundu ali ndi misala. 8Babulo wagwa dzidzidzi
naonongedwa; mumkuwire iye; mutengere zowawa zace bvunguti,
kapena angacire. 9Tikadaciritsa Babulo koma sanacire; mumsiye
iye, tipite tonse yense ku dziko lace; pakuti ciweruziro cace cifikira
kumwamba, cinyamulidwa mpaka kuthambo, 10Yehova waturutsa
cilungamo cathu; tiyeni tilalikire m'Ziyoni nchito ya Yehova Mulungu
wathu. 11Nolani mibvi; gwirani zolimba zikopa; Yehova waukitsa
mtima wa mafumu a Amedi; cifukwa alingalirira Babulo kuti
amuononge; pakuti ndi kubwezera cilango kwa Yehova; kubwezera
cilango cifukwa ca Kacisi wace. 12Muwakwezere mbendera makoma
a Babulo, mulimbikitse ulonda, muike alonda, mupangiretu olalira,
pakuti Yehova waganiziratu ndi kucita comwe ananena za okhala
m'Babulo. 13Iwe wokhala pa madzi ambiri, wocuruka cuma,
cimariziro cako cafika, cilekezero ca kusirira kwako. 14Yehova wa
makamu walumbira pa Iye mwini, kuti, Ndithu ndidzakudzaza iwe
ndi anthu, monga ndi madzombe; ndipo adzakukwezera iwe mpfuu.
15Iye analenga dziko lapansi ndi mphamvu yace, wakhazika dziko
lapansi ndi nzeru yace, ndi luso anayala thambo; 16pamene Iye
anena mau, pali unyinji wa madzi m'mwamba, ndipo akweretsa
nkhungu ku malekezero a dziko lapansi, ayesa mphezi ya mvula,
aturutsa mphepo ya m'nyumba za cuma zace. 17Anthu onse ali
opulukira ndi opanda nzeru; wakusula golidi acitidwa manyazi ndi
fanizo lace losema; pakuti fanizo lace loyenga liri bodza, mulibe
mpweya m'menemo. 18Ngwacabe, ciphamaso; nthawi
yakulangidwa kwao adzatayika. 19Gawo la Yakobo silifanafana ndi
izo; pakuti Iye ndiye analenga zonse; Israyeli ndi mtundu wa
colowa cace, dzina lace ndi Yehova wa makamu.
20Iwe ndiwe cibonga canga ndi zida zanga za nkhondo; ndi iwe
ndidzatyolatyola amitundu, ndi iwe ndidzaononga maufumu; 21ndi

iwe ndidzatyolatyola kavalo ndi wakwera wace; 22ndi iwe ndidzatyolatyola gareta ndi iye wokweramo; ndi iwe ndidzatyolatyola mwamuna ndi mkazi; ndi iwe ndidzatyolatyola wokalamba ndi mnyamata; ndi iwe ndidzatyolatyola mnyamata ndi namwali; 23ndi iwe ndidzatyolatyola mbusa ndi zoweta zace; ndi iwe ndidzatyolatyola wakulima ndi gori la ng'ombe lace; ndi iwe ndidzatyolatyola akazembe ndi ziwanga, 24Ndipo ndidzabwezera Babulo ndi okhala m'Kasidi zoipa zao zonse anazicita m'Ziyoni pamaso panu, ati Yehova.
25Taona, ndimenyana ndi iwe, iwe phiri lakuononga, ati Yehova, limene liononga dziko lonse; ndipo ndidzakutambasulira iwe dzanja langa, ndipo ndidzakugubuduza iwe kumatanthwe, ndipo ndidzakuyesa iwe phiri lotenthedwa. 26Ndipo sadzacotsa pa iwe mwala wa pangondya, kapena mwala wa pamaziko; koma udzakhala bwinja nthawi zonse, ati Yehova. 27Kwezani mbendera m'dziko, ombani lipenga mwa amitundu, konzerani amitundu amenyane naye, mummemezere maufumu a Ararati, Mini, ndi Asikenaza; muike nduna; amenyane naye; mukweretse akavalo ngati mandowa. 28Konzerani amitundu amenyane ndi iye, mafumu a Amedi, akazembe ace, ndi ziwanga zace zonse, ndi dziko lonse la ufumu wace. 29Dziko linthunthumira ndi kuphwetekedwa, pakuti zimene Yehova analingalirira Babulo ziripobe, zoti ayese dziko la Babulo bwinja lopanda wokhalamo. 30Olimba a ku Babulo akana kumenyana, akhala m'malinga ao; mphamvu yao yalephera; akhala ngati akazi; nyumba zace zapsya ndi moto; akapici ace atyoka. 31Wamtokoma mmodzi adzathamanga kukakomana ndi mnzace, ndi mthenga mmodzi kukomana ndi mnzace, kukauza mfumu ya ku Babulo kuti mudzi wace wagwidwa ponsepo; 32pamadooko patsekedwa, pamatamanda a mabango patenthedwa ndi moto, ndi anthu a nkhondo aopa.
33Pakuti atero Yehova wa makamu, Mulungu wa Israyeli: Mwana wamkazi wa Babulo akunga dwale pamene aliunda; patsala kanthawi kakang'ono, ndipo nthawi yamasika idzamfikira iye. 34Nebukadirezara mfumu ya ku Babulo wandidya ine, wandiphwanya ine, wandiyesa ine ngati mbiya yopanda kanthu, wandimeza ngati ng'ona, wadzaza m'kamwa mwace ndi zotsekemera zanga, wanditaya ine, 35Wokhala m'Ziyoni adzati, Ciwawa anandicitira ine ndi thupi langa cikhale pa Babulo; nadzati Yerusalemu, Mwazi wanga ukhale pa okhala m'Kasidi. 36Cifukwa cace Yehova atero: Taona, ndidzanenera iwe mlandu wako, ndidzawabwezera cilango cifukwa ca iwe; ndidzaphwetsa nyanja yace, ndidzaphwetsa citsime cace. 37Ndipo Babulo adzasanduka miunda, mokhala ankhandwe, cizizwitso, cotsonyetsa, wopanda okhalamo. 38Adzabangula pamodzi ngati misona ya mikango;

adzacita nthulu ngati ana a mikango. 39Pamene atentha,
ndidzakonza madyerero ao, ndidzawaledzeretsa, kuti asangalale,
agone cigonere, asanyamuke, ati Yehova. 40Ndidzawagwetsa kuti
aphedwe manga nkhosa zamphongo, ndi atonde. 41Sesake
wagwidwatul cimene dziko lonse lapansi linacitamanda calandidwa
dzidzidzi Babulo wakhalatu bwinja pakati pa amitundu 42Nyanja
yakwera kufikira ku Babulo; wamira ndi mafunde ace
aunyinji. 43Midzi yace yakhala bwinja, dziko louma, cipululu
mosakhalamo anthu, mosapita mwana wa munthu ali
yense. 44Ndipo Ine ndiweruza Beli m'Babulo, ndipo ndidzaturutsa
m'kamwa mwace comwe wacimeza; ndipo amitundu
sadzasonkhaniranso konse kwa iye; inde, khoma la Babulo
lidzagwa.
45Anthu anga, turukani pakati pace, mudzipulumutse munthu
yense ku mkwiyo waukali wa Yehova. 46Mtima wanu usalefuke,
musaope cifukwa ca mbiri imene idzamveka m'dzikomu; pakuti
mbiri idzafika caka cina, pambuyo pace caka cina mbiri yina, ndi
ciwawa m'dziko, wolamulira kumenyana ndi wolamulira. 47Cifukwa
cace, taonani, masiku alinkudza, amene ndidzaweruza mafano
osemasema a Babulo, ndipo dziko lace lonse lidzakhala ndi
manyazi; ndipo ophedwa ace onse adzagwa pakati
pace. 48Pamenepo kumwamba ndi dziko lapansi, ndi zonse ziri
m'menemo, zidzayimba mokondwerera Babulo; pakuti akufunkha
adzafika kwa iye kucokera kumpoto, ati Yehova. 49Monga Babulo
wagwetsa ophedwa a Israyeli, momwemo pa Babulo padzagwa
ophedwa a dziko lonse. 50Inu amene mwapulumuka kulupanga,
pitani inu, musaime ciimire; mukumbukire Yehova kutari,
Yerusalemu alowe m'mtima mwanu. 51Tiri ndi manyazi, cifukwa
tamva mnyozo; manyazi aphimba nkhope zathu; pakuti alendo
alowa m'malo opatulika a nyumba ya Yehova. 52Cifukwa cace,
taona, masiku alinkudza, ati Yehova, amene ndidzaweruza mafano
ace; ndipo pa dziko lace lonse olasidwa adzabuula. 53Ngakhale
Babulo adzakwera kumwamba, ngakhale adzalimbitsa msanje wa
mphamvu yace, koma kucokera kwa Ine akufunkha adzafika kwa
iye, ati Yehova. 54Mau akupfuula ocokera ku Babulo, ndi a
cionongeko cacikuru ku dziko la Akasidi! 55pakuti Yehova afunkha
Babulo, aononga m'menemo mau akuru; ndipo mafunde ace
adzakokoma ngati madzi ambiri, mau ao aphokosera; 56pakuti
wakufunkha wafika kwa iye, kwa Babulo, ndi anthu ace olimba
agwidwa, mauta ao atyokatyoka, pakuti Yehova ndiye Mulungu
wakubwezera, adzabwezera ndithu. 57Ndipo ndidzaledzeretsa
akuru ace ndi anzeru ace, akazembe ace ndi ziwanga zace, ndi
anthu ace olimba; ndipo adzagona cigonere, sadzanyamuka, ati
Mfumu, dzina lace ndi Yehova wa makamu. 58Yehova wa makamu

atero: Makoma otakata a Babulo adzagwetsedwa ndithu, ndi zitseko zace zazitari zidzatenthedwa ndi moto; anthu adzagwirira nchito cabe, ndi mitundu ya anthu idzagwirira moto, nidzatopa.
59Mau amene Yeremiya mneneri anauza Seraya mwana wa Neriya, mwana wa Maseya, pamene iye ananka ndi Zedekiya mfumu ya Yuda ku Babulo caka cacinai ca ufumu wace. Ndipo Seraya anali kapitao wa cigono cace. 60Ndipo Yeremiya analemba m'buku coipa conse cimene cidzafika pa Babulo, mau onse awa olembedwa za Babulo. 61Ndipo Yeremiya anati kwa Seraya, Pamene ufika ku Babulo, samalira kuti uwerenge mau awa onse, 62nuti, inu Yehova, mwanena za malo ano, kuti mudzawatha, kuti asakhalemo, ngakhale anthu ngakhale nyama, koma akhale bwinja nthawi za nthawi. 63Ndipo padzakhala, utatha kuwerenga buku ili, Ib ulimange ndi mwala, nuliponye pakati pa Firate; 64nuti, Comweco adzamira Babulo, sadzaukanso cifukwa ca coipa cimene ndidzamtengera iye; ndipo adzatopa.
Mau a Yeremiya ndi omwewo.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Yerusalemu amangidwa misasa, nalandidwa, napasulidwa

1Zedekiya anali wa zaka makumi awiri kudza cimodzi pamene
analowa ufumu wace; ndipo analamulira m'Yerusalemu zaka khumi
kudza cimodzi; dzina la amace ndi Hamutala mwana wamkazi wa
Yeremiya wa ku Libina. 2Ndipo iye anacita zoipa pamaso pa
Yehova, monga mwa zonse anazicita Yehoyakimu. 3Pakuti zonse
zinacitika m'Yerusalemu ndi m'Yuda cifukwa ca mkwiyo wa Yehova,
mpaka anawacotsa pamaso pace; ndipo Zedekiya anampandukira
mfumu ya Babulo. 4Ndipo panaoneka caka cacisanu ndi cinai ca
ufumu wace mwezi wakhumi, tsiku lakhumi la mwezi,
Nebukadirezara mfumu ya ku Babulo anafika, iye ndi nkhondo
yace, kuti amenyane ndi Yerusalemu, ndipo anammangira zitando;
ndipo anammangira malinga pozungulira pace. 5Ndipo mudzi
unazingidwa mpaka caka ca khumi ndi cimodzi ca mfumu
Zedekiya. 6Mwezi wacinai, tsiku lacisanu ndi cinai la mwezi, njala
inabvuta m'mudzi, ndipo anthu a m'dziko analibe
zakudya. 7Pamenepo anaboola mudzi, ndipo anathawa amuna
onse a nkhondo, naturuka m'mudzi usiku pa njira ya kucipata ca
pakati pa makoma awiri, imene inali pa munda wa mfumu; Akasidi
alikumenyana ndi mudzi pozungulira pace, ndipo anapita njira ya
kucidikha. 8Koma nkhondo ya Akasidi inamtsata mfumu, nimpeza
Zedekiya m'zidikha za ku Yeriko; ndipo nkhondo yace yonse
inambalalikira iye. 9Ndipo anamgwira iye, namtengera kwa mfumu
ya ku Babulo ku Ribila m'dziko la Hamati; ndipo iye
anamweruza. 10Ndipo mfumu ya ku Babulo inapha ana a Zedekiya
pamaso pace; niphanso akuru onse a Yuda m'Ribila. 11Ndipo
anakolowola maso a Zedekiya, ndipo mfumu ya ku Babulo
inammanga m'zigologolo, nimtengera ku Babulo, nimuika
m'ndende mpaka tsiku la kufa kwace.
12Mwezi wacisanu, tsiku lakhumi la mwezi, ndico caka cakhumi ndi
cisanu ndi cinai ca Nebukadirezara, mfumu ya ku Babulo, analowa
m'Yerusalemu Nebuzaradani kapitao wa alonda, amene anaimirira
pamaso pa mfumu ya ku Babulo: 13ndipo anatentha nyumba ya
Yehova ndi nyumba ya mfumu, ndi nyumba zonse za
m'Yerusalemu, ngakhale zinyumba zazikuru zonse, anazitentha ndi
moto. 14Ndipo nkhondo yonse ya Akasidi, imene inali ndi kapitao
wa alonda, inagumula makoma onse a Yerusalemu pomzungulira
pace. 15Ndipo Nebuzaradani kapitao wa alonda anatenga ndende
anthu aumphawi, ndi anthu otsala amene anatsala m'mudzi, ndi
amene anapandukira, kutsata mfumu ya ku Babulo, ndi otsala a
unyinjiwo. 16Koma Nebuzaradani kapitao wa alonda anasiya
aumphawi a padziko akhale akulima mphesa ndi akulima
m'minda. 17Ndi mizati yamkuwa imene inali m'nyumba ya Yehova,

ndi zoikapo ndi thawale lamkuwa zimene zinali m'nyumba ya Yehova, Akasidi anazityolatyola, nanka nao mkuwa wace wonse ku Babulo. 18Ndiponso miphika, ndi zoolera, ndi mbano zao, ndi mbale, ndi zipande, ndi zipangizo zonse zamkuwa zimene anatumikira nazo, anazicotsa. 19Ndi zikho, ndi zopalira moto, ndi mbale, ndi miphika, ndi zoikapo nyali, ndi zipande, ndi mitsuko; ndi golidi, wa zija zagolidi, ndi siliva, wa zija zasiliva, kapitao wa alonda anazicotsa. 20Nsanamira ziwirizo, thawale limodzilo, ndi ng'ombe zamkuwa zinali pansi pa zoikapo, zimene mfumu Solomo anazipangira nyumba ya Yehova; mkuwa wa zipangizo zonsezi sanatha kuyesa kulemera kwace. 21Koma nsanamirazo, utari wace wa nsanamira yina unafikira mikono khumi mphambu isanu ndi itatu; ndi cingwe ca mikono khumi ndi iwiri cinaizinga; kucindikira kwace kunali zala zinai; inali yagweregwere. 22Ndipo korona wamkuwa anali pamwamba pace; utari wace wa korona mmodzi unali wa mikono isanu, ndi made ndi makangaza pakorona pozungulira pace, onse amkuwa: nsanamira inzace yomwe inali nazo zonga zomwezi, ndi makangaza. 23Ndipo pambali pace panali makangaza makumi asanu ndi anai kudza asanu ndi limodzi; ndipo makangaza onse anali zana limodzi pamade pozungulira pace. 24Ndipo kapitao wa alonda anatenga Seraya mkuru wansembe, ndi Zefaniya wansembe waciwiri, ndi akudikira pakhomo atatu; 25ndipo m'mudzi anatenga kazembe amene anali woyang'anira anthu a nkhondo ndi amuna asanu ndi awiri a iwo akuona nkhope ya mfumu, amene anapezedwa m'mudzi; ndi mlembi wa kazembe wa nkhondo, amene akamemeza anthu a m'dziko; ndi amuna makumi asanu ndi limodzi a anthu a m'dziko, amene anapezedwa pakati pa mudzi. 26Ndipo Nebuzaradani kapitao wa alonda anatenga iwo, nadza nao kwa mfumu ya ku Babulo ku Ribila. 27Ndipo mfumu ya ku Babulo anawakantha, nawapha pa Ribila m'dziko la Hamati. Comweco Yuda anatengedwa ndende kuturuka m'dziko lace. 28Amenewa ndi anthu amene Nebukadirezara anatenga ndende: caka cacisanu ndi ciwiri, Ayuda zikwi zitatu kudza makumi awiri ndi atatu; 29caka cakhumi ndi cisanu ndi citatu ca Nebukadirezara iye anatenga ndende kucokera m'Yerusalemu anthu mazana asanu ndi atatu kudza makumi atatu ndi awiri; 30caka ca makumi awiri ndi zitatu ca Nebukadirezara Nebuzaradani kapitao wa alonda anatenga ndende Ayuda mazana asanu ndi awiri kudza makumi anai ndi asanu; anthu onse anali zikwi zinai kudza mazana asanu ndi limodzi.
31Ndipo panali caka ca makumi atatu ndi zisanu ndi ziwiri ca undende wa Yehoyakimu mfumu ya Yuda, mwezi wakhumi ndi iwiri, tsiku la makumi awiri ndi asanu la mwezi, Evili-Merodaki mfumu ya ku Babulo anaweramutsa mutu wa Yehoyakimu mfumu ya Yuda,

namturutsa iye m'ndende; 32nanena naye bwino, naika mpando
wace upose mipando ya mafumu amene anali naye
m'Babulo. 33Ndipo anapindula zobvala zace za m'ndende, ndipo
sanaleka kudya pamaso pace masiku onse a moyo wace. 34Koma
phoso lace mfumu ya ku Babulo sanaleka kumpatsa, phoso tsiku
ndi tsiku gawo lace, mpaka tsiku la kufa kwace, masiku onse a
moyo wace.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Lametations

Maliro 1

Tsoka la Yerusalemu

1Ha! mudziwo unadzala anthu, ukhalatu pa wokha!
Ukunga mkazi wamasiye!
Waukuruwo mwa amitundu, kalonga wamkazi m'madera a dziko
Wasanduka wolamba!
2Uliralira usiku; misozi yace iri pa masaya ace;
Mwa onse amene anaukonda mulibe mmodzi wakuutonthoza:
Mabwenzi ace onse aucitira ziwembu,
Asanduka adani ace.
3Yuda watengedwa ndende cifukwa ca msauko ndi ukapolo waukuru;
Akhala mwa amitundu, sapeza popuma;
Onse akumlondola anampeza pakati popsinjikiza.
4M'njira za Ziyoni mulira posoweka akudzera msonkhano;
Pa zipata zace zonse papasuka; ansembe ace onse ausa moyo;
Anamwali ace asautsidwa; iye mwini namva zowawa.
5Amaliwongo ace asanduka akuru ace, adani ace napindula;
Pakuti Yehova wamsautsa pocuruka zolakwa zace;
Ana ace ang'ono alowa m'ndende pamaso pa adani ace.
6Ulemu wace wonse wamcokera mwana wamkazi wa Ziyoni;
Akalonga ace asanduka nswala zosapeza busa,
Anayenda opanda mphamvu pamaso pa wompitikitsa.
7M'masiku a msauko wace ndi kusocera kwace
Yerusalemu ukumbukira zokondweretsa zace zonse zacikhalire;
Pogwidwa anthu ace ndi mdaniyo popanda wakuupulumutsa,
Adaniwo anamuona naseka mwacipongwe mabwinja ace.
8Yerusalemu wacimwa kwambiri; cifukwa cace wasanduka cinthu conyansa;
Onse akuulemekeza aupeputsa, pakuti auona wamarisece;
Inde, uusa moyo, nubwerera m'mbuyo.
9Udio wace unali m'nsaru zace; sunakumbukira citsiriziro cace;
Cifukwa cace watsika mozizwitsa; ulibe wakuutonthoza;
Taonani Yehova, msauko wanga, pakuti mdaniyo wadzikuzayekha.
10Amaliwongo atambasulira manja ao pa zokondweretsa zace zonse;
Pakuti waona amitundu atalowa m'malo ace opatulika,
Amene munalamulira kuti asalowe mumsonkhano mwanu.
11Anthu ace onse ausa moyo nafunafuna mkate;
Ndi zokondweretsa zao agula zakudya kuti atsitsimutse moyo wao;
Taonani, Yehova, nimupenye; pakuti ndasanduka wonyansa.
12Kodi muyesa cimeneci cabe, nonsenu opita panjira?

Penyani nimuone, kodi ciripo cisoni cina ngati cangaci amandimvetsa ine,
Cimene Yehova wandisautsa naco tsiku la mkwiyo wace waukali?
13Anatumiza moto wocokera kumwamba kulowa m'mafupa anga, unawagonjetsa;
Wachera mapazi anga ukonde, wandibwezera m'mbuyo;
Wandipululutsa ndi kundilefula tsiku lonse.
14Gori la zolakwa zanga lamangidwa ndi dzanja lace;
Zalukidwa, zakwera pakhosi panga; iye wakhumudwitsa mphamvuyanga;
Ambuye wandipereka m'manja mwao, sindithai kuwalaka.
15Ambuye wapepula ngwazi zanga zonse pakati panga;
Waitanira msonkhano pa ine kuti uphwanye anyamata anga,
Ambuye wapondereza namwaliyo, mwana wamkazi wa Ziyoni, monga mopondera mphesa.
16Cifukwa ca zimenezi ndilira; diso langa, diso langatu likudza madzi:
Pakuti wonditonthoza, wotsitsimutsa moyo wanga, anditarikira;
Ana anga asungulumwa, pakuti adaniwo apambana.
17Ziyoni atambasula manja ace, palibe wakumtonthoza;
Yehova walamulira kuti omzungulira Yakobo akhale adani ace;
Yerusalemu wasanduka cinthu conyansa pakati pao.
18Yehova ali wolungama; pakuti ndapikisana ndi m'kamwa mwace:
Mudtvetu, mitundu ya anthu nonsenu, nimuone cisoni canga;
Anamwali ndi anyamata anga atha kulowa m'ndende.
19Ndinaitanaakundikondawokoma anandinyenga;
Ansembe ndi akulu anga anamwalira m'mudzimu,
Alikufunafuna zakudya zotsitsimutsa miyoyo yao.
20Onani, Yehova; pakuti ndabvutika, m'kati mwanga mugwedezeka;
Mtima wanga wasanduka mwa ine; pakuti ndapikisana nanu ndithu;
Kunjako lupanga limangopha ana; m'nyumba muli imfa.
21Iwo anamva kuti ndiusa moyo, palibe wonditonthoza;
Adani anga onse atha kumva msauko wanga, nakondwera kuti mwatero ndinu;
Mudzafikitsa tsiku lija mwalichula, ndipo iwowo adzanga ine.
22Zoipa zao zonse zidze pamaso panu,
Muwacitire monga mwandicitira ine cifukwa ca zolakwa zanga zonse,
Pakuti ndiusa moyo kwambiri, ndi kulefuka mtima wanga,

©The Bible Society of Malawi, 1992

Yerusalemu amangidwa misasa, njala isautsa, mudzi upasuka

1Ambuye waphimbatu ndi mtambo mwana wamkazi wa Ziyoni,
pomkwiyira!
Wagwetsa pansi kucokera kumwamba kukoma kwace kwa Israyeli;
Osakumbukira poponda mapazi ace tsiku la mkwiyo wace.
2Yehova wameza nyumba zonse za Yakobo osazicitira cisoni;
Wagumula malinga a mwana wamkazi wa Yuda mwa ukali wace;
Wawagwetsera pansi, waipitsa ufumuwo ndi akalonga ace.
3Pokwiya moopsya walikha nyanga zonse za Israyeli;
Wabweza m'mbuyo dzanja lace lamanja pamaso pa adaniwo,
Natentha Yakobo ngati moto wamalawi wonyambita mozungulira.
4Wathifula uta wace ngati mdani, waima ndi dzanja lace lamanja
ngati mmaliwongo;
Wapha onse okondweretsa maso;
Watsanulira ukali wace ngati moto pa hema wa mwana wamkazi wa
Ziyoni.
5Yehova wasanduka mdani, wameza Israyeli;
Wameza zinyumba zace zonse, wapasula malinga ace;
Nacurukitsira mwana wamkazi wa Yuda maliro ndi cibumo.
6Wacotsa mwamphamvu dindiro lace ngati la m'munda;
Waononga mosonkhanira mwace;
Yehova waiwalitsa anthu msonkhano ndi sabata m'Ziyoni;
Wanyoza mfumu ndi wansembe mokwiya mwaukali.
7Ambuye wataya guwa lace la nsembe, malo ace opatulika
amnyansira;
Wapereka m'manja a adani ace makoma a zinyumba zace;
Iwo anaphokosera m'nyumba ya Yehova ngati tsiku la msonkhano.
8Yehova watsimikiza mtima kupasula linga la mwana wamkazi wa
Ziyoni;
Watambalika cingwe, osabweza dzanja lace kuti lisaonongepo;
Waliritsa chemba ndi linga; zilefuka pamodzi.
9Zipata zace zalowa pansi; waononga ndi kutyola mipiringidzo
yace;
Mfumu yace ndi akalonga ace ali pakati pa amitundu akusowa
cilamulo;
Inde, aneneri ace samalandira masomphenya kwa Yehova.
10Akulu a mwana wamkazi wa Ziyoni akhala pansi natonthola;
Aponya pfumbi pa mitu yao, namangirira ciguduli m'cuuno mwao:
Anamwali a ku Yerusalemu aweramitsa pansi mitu yao.
11Maso anga alefuka ndi misozi, m'kati mwanga mugwedezeka;
Ciwindi canga cagwa pansi cifukwa ca kupasuka kwa mwana
wamkazi wa anthu amtundu wanga;

Cifukwa tiana ndi oyamwa akomoka m'makwalala a mudziwu.
12Amati kwa amao, Tirigu ndi vinyo ali kuti?
Pokomoka iwo ngati olasidwa m'makwalala a mudziwu,
Potsanulidwa miyoyo yao pa zifuwa za amao.
13Ndikucitire umboni wotani? ndikuyerekeze ndi ciani, mwana wamkazi wa Yerusalemu?
Ndikulinganize ndi ciani kuti ndikutonthoze, namwaliwe, mwana wamkazi wa Ziyoni?
Popeza akula ngati nyanja; ndani angakucize?
14Aneneri ako anakuonera masomphenya acabe ndi opusa;
Osaulula mphulupulu yako kuti abweze undende wako,
Koma anakuonera manenero acabe ndi opambutsa.
15Onse opita panjira akuombera manja:
Atsonya, napukusira mitu yao pa mwana wamkazi wa Yerusalemu, nati,
Kodi uwu ndi mudzi wochedwa wokongola, wangwiro, wokondweretsa dziko lonse?
16Adani ako onse ayasamira pa iwe, Atsonya nakukuta mano, nati, Taumeza;
Ndithu ili ndi tsiku tinaliyembekezalo, talipeza, taliona.
17Yehova wacita comwe analingalira;
Watsiriza mau ace, amene analamulira nthawi yakale;
Wagwetsa osacitira cisoni;
Wakondweretsa adani pa iwe,
Wakweza nyanga ya amaliwongo ako.
18Mtima wao unapfuula kwa Ambuye,
Linga iwe la mwana wamkazi wa Ziyoni, igwe misozi ngati mtsinje usana ndi usiku;
Usapume kanthawi, asaleke mwana wa diso lako.
19Tauka, tapfuula usiku, poyamba kulonda;
Tsanulira mtima wako ngati madzi pamaso pa Ambuye;
Takwezera maso ako kwa Iye, cifukwa ca moyo wa tiana tako,
Timene tilefuka ndi njala pa malekezero a makwalala onse.
20Onani Yehova, nimupenye, mwacitira ayani ici?
Kodi akazi adzadya zipatso zao, kunena ana amene anawaseweza?
Kodi wansembe ndi mneneri adzaphedwa m'malo opatulika a Ambuye?
21Wamng'ono ndi nkhalamba agona pansi m'makwalala;
Anamwali ndi anyamata anga agwa ndi lupanga;
Munawapha tsiku la mkwiyo wanu, munawagwaza osacitira cisoni.
22Mwaitana zondiopsya mozungulira ngati tsiku la msonkhano;
Panalibe wopulumuka ndi wotsala tsiku la mkwiyo wa Yehova;
Omwe ndinawaseweza ndi kuwalera, adaniwo anawatsiriza.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Ezekiel

Ezekieli 1

Masomphenya a Ezekieli

1NDIPO kunali caka ca makumi atatu, mwezi wacinai, tsiku lacisanu
la mwezi, pokhala ine pakati pa andende kumtsinje Kebara,
kunatseguka kumwamba, ndipo ndinaona masomphenya a
Mulungu. 2Tsiku lacisanu la mwezi, ndico caka cacisanu ca
kutengedwa ndende mfumu Yoyakini, 3anadzadi mau a Yehova kwa
Ezekieli wansembe, mwana wa Buzi, m'dziko la Akasidi kumtsinje
Kebara; ndi pomwepo dzanja la Yehova lidamkhalira. 4Ndinapenya,
ndipo taonani, mkuntho wa mphepo wocokera kumpoto, mtambo
waukuru ndi moto wopfukusika m'mwemo, ndi pozungulira pace
padacita ceza, ndi m'kati mwace mudaoneka ngati citsulo cakupsa
m'kati mwa moto. 5Ndi m'kati mwace mudaoneka mafaniziro a
zamoyo zinai. Ndipo maonekedwe ao ndiwo anafanana ndi
munthu, 6ndi yense anali nazo nkhope zinai, ndi yense wa iwo
anali nao mapiko anai. 7Ndi mapazi ao anali mapazi oongoka, ndi
ku mapazi ao kunanga kuphazi kwa mwana wa ng'ombe; ndipo
ananyezimira ngati mawalidwe a mkuwa wowalitsidwa. 8Zinali
naonso manja a munthu pansi pa mapiko ao pa mbali zao zinai;
ndipo zinaizi zinali nazo nkhope zao ndi mapiko ao. 9Mapiko ao
analumikizana; sizinatembenuka poyenda; ciri conse cinayenda ndi
kulunjika kutsogoloko. 10Mafaniziro a nkhope zao zinali nayo
nkhope ya munthu; ndi izi zinai zinali nayo nkhope ya mkango pa
mbali ya ku dzanja lamanja; ndi izi zinai zinali nayo nkhope ya
ng'ombe pa mbali ya ku dzanja lamanzere; izi zinai zinali nayonso
nkhope ya ciombankhanga. 11Ndi nkhope zao ndi mapiko ao
zinagawikana kumutu; ciri conse cinali nao mapiko awiri
olumikizana, ndi awiri anaphimba thupi. 12Ndipo zinayenda, ciri
conse cinalunjika kutsogolo kwace uko mzimu unafuna kumukako
zinamuka, sizinatembenuka poyenda. 13Kunena za mafaniziro a
zamoyozo, maonekedwe ao ananga makara amoto, monga
maonekedwe a miyuni; motowo unayendayenda pakati pa
zamoyozo, ndi motowo unacita ceza, ndi m'motomo mudaturuka
mphezi. 14Ndipo zamoyozo zinathamanga ndi kubwerera, ngati
maonekedwe a mphezi yong'anima. 15Ndipo pakupenyerera ine
zamoyozo, taonani, njinga imodzi imodzi yoponda pansi pafupi ndi
zamoyozo pa nkhope zao zinai. 16Maonekedwe a njingazi ndi
mapangidwe ao ananga mawalidwe a berulo; ndi izi zinai
zinafanana mafaniziro ao; ndi maonekedwe ao ndi mapangidwe ao
anali ngati njinga ziwiri zopingasitsana. 17Poyenda zinayenda ku
mbali zao zinai, zosatembenuka poyenda. 18Ndi mikombero yace
inali yokuzika ndi yoopsa; ndi izi zinai zinali ndi mikombero yao

yodzala ndi maso pozungulira pao. 19Ndipo poyenda zamoyozo, njingazi zinayenda pambali pao; ndipo ponyamuka pansi zamoyozo, njinga zinanyamuka. 20Kuli konse mzimu ukuti umuke, zinamuka komwe mzimu ukuti umuke; ndi njingazi zinanyamuka pambali pa izo; pakuti mzimu wa zamoyozo unali m'njingazo. 21Poyenda zija zinayenda izi, poima zija zinaima izi; ndipo ponyamuka pansi zija njingazi zinanyamuka pambali pa izo; pakuti mzimu wa zamoyozo unali mu njingazi. 22Ndi pa mitu ya zamoyozi panali cifaniziro ca thambo, monga mawalidwe a krustalo woopsa, loyalika pamwamba pamitu pao. 23Ndi pansi pa thambolo mapiko ao analunjikana, lina kulunjika ku linzace; ciri conse cinali nao mapiko awiri akuphimba matupi ao, cakuno ndi cauko. 24Ndipo pakuyenda izi ndinamva mkokomo wa mapiko ao, ngati mkokomo wa madzi akulu, ngati mau a Wamphamvuyonse, phokoso lakusokosera ngati phokoso la ankhondo; pakuima zinagwetsa mapiko ao. 25Ndipo panamveka mau pamwamba pa thambolo linali pamwamba pa mitu yao; pakuima izi zinagwetsa mapiko ao. 26Ndi pamwamba pa thambo linali pamitu pao panali cifaniziro ca mpando wacifumu, maonekedwe ace ngati mwala wa safiro; ndipo pa cifaniziro ca mpando wacifumu panali cifaniziro ngati maonekedwe ace a munthu wokhala pamwamba pace. 27Ndipo ndinapenya ngati citsulo cakupsa, ngati maonekedwe ace a moto m'kati mwace pozungulira pace, kuyambira maonekedwe a m'cuuno mwace ndi kumwamba kwace; ndipo kuyambira maonekedwe a m'cuuno mwace ndi kunsi kwace ndinaona ngati maonekedwe ace a moto; ndi kunyezimira kudamzinga. 28Ngati maonekedwe a utawaleza uli m'mtambo tsiku la mvula, momwemo maonekedwe a kunyezimira kwace pozungulira pace. Ndiwo maonekedwe a cifaniziro ca ulemerero wa Yehova. Ndipo pakucipenya ndinagwa nkhope pansi, ndipo ndinamva mau a wina wakunena.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Kuitanidwa kwa Ezekieli

1Ndipo anati kwa ine, Wobadwa ndi munthu iwe, khala ciriri, ndipo
ndidzanena nawe. 2Ndipo unandilowa mzimu pamene ananena
nane, ndi kundiimika ndikhale ciriri; ndipo ndinamumva Iye
wakunena nane. 3Nati kwa ine, Wobadwa ndi munthu iwe,
ndikutumizira kwa ana a Israyeli, kwa mitundu ya anthu opanduka,
amene anapandukana nane; iwo ndi makolo ao anandilakwira
mpaka lero lomwe. 4Ndipo anawa, ndiwo acipongwe ndi ouma
mtima, ndikutumiza kwa iwo; ndipo ukanene nao, Atero Yehova
Mulungu. 5Ndipo iwowa, ngakhale akamva kapena akaleka kumva,
(pakuti ndiwo nyumba yopanduka,) koma adzadziwa kuti panali
mneneri pakati pao. 6Ndipo iwe, wobadwa ndi munthu iwe,
usawaopa, kapena kuopa mau ao; ingakhale mitungwi ndi minga
ikhala ndi iwe, nukhala pakati pa zinkhanira, usaopa mau ao
kapena kuopsedwa ndi nkhope zao; pakuti ndiwo nyumba
yopanduka. 7Ndipo ukanene nao mau anga, ngakhale akamva
kapena akaleka kumva; pakuti iwo ndiwo opanduka. 8Koma iwe,
wobadwa ndi munthu, tamvera ici ndirikunena nawe; usakhale
iwewopanduka, ngati nyumba ija yopanduka; tsegula pakamwa
pako, nudye comwe ndikupatsa. 9Ndipo pakupenya ine ndinaona
dzanja londiturutsira, ndipo taonani, mpukutu wa buku
m'mwemo; 10naufunyulula pamaso panga; ndipo unalembedwa
m'kati ndi kubwalo; munalembedwa m'mwemo nyimbo za maliro,
ndi cisoni, ndi tsoka.

©The Bible Society of Malawi, 1992

1Ndipo ananena nane, Wobadwa ndi munthu iwe, Idya cimene
wacipeza; idya mpukutu uwu, numuke ndi kunena ndi nyumba ya
Israyeli. 2Pamenepo ndinatsegula pakamwa panga ndipo
anandidyetsa mpukutuwo. 3Nati kwa ine, Wobadwa ndi munthu iwe,
dyetsa m'mimba mwako, nudzaze matumbo ako ndi mpukutu uwu
ndakupatsawu. M'mwemo ndinaudya, ndi m'kamwa mwanga
munazuna ngati uci.
4Ndipo anati kwa ine, Wobadwa ndi munthu iwe, Muka, nufike kwa
nyumba ya Israyeli, nunene nao mau anga. 5Pakuti sutumizidwa
kwa anthu a cinenedwe cosamveka ndi cobvuta, koma kwa
nyumba ya Israyeli; 6si kwa mitundu yambiri ya anthu a cinenedwe
cosamveka ndi cobvuta, amene sukhoza kudziwitsa cinenedwe
cao. Zedi ndikakutumiza kwa iwowa adzamvera iwe. 7Koma
nyumba ya Israyeli siidzakumvera, pakuti siifuna kundimvera Ine;
pakuti nyumba yonse ya Israyeli ndiyo yolimba mutu ndi youma
mtima. 8Taona ndakhwimitsa nkhope yako itsutsane nazo nkhope
zao; ndalimbitsanso mutu wako utsutsane nayo mitu
yao. 9Ndalimbitsa mutu wako woposa mwala wolimbitsitsa,
usawaopa kapena kutenga nkhawa pamaso pao; pakuti iwo ndiwo
nyumba yopanduka. 10Ananenanso nane, Wobadwa ndi munthu
iwe, mau anga onse ndidzawanena ndi iwe uwalandire m'mtima
mwako, utawamva m'makutu mwako. 11Numuke, nufike kwa
andende kwa ana a anthu a mtundu wako, nunene nao ndi
kuwauza, Atero Yehova Mulungu, ngakhale akamva kapena akaleka
kumva.
12Pamenepo mzimu unandinyamula, ndipo ndinamva kumbuyo
kwanga mau a mkokomo waukuru, ndi kuti, Wodala ulemerero wa
Yehova m'malo mwace. 13Ndipo ndinamva mkokomo wa mapiko a
zamoyozo pakukhudzana, ndi mlikiti wa njingazo m'mbali mwa izo,
ndilo phokoso la mkokomo waukuru. 14M'mwemo mzimu
unandinyamula ndi kucoka nane; ndipo ndinamuka wowawidwa,
womyuka mtima; koma dzanja la Yehova linandigwirizitsa, 15Ndipo
ndinafika kwa andende ku Telabibu, okhala kumtsinje Kebara, ndiko
kwao; ndipo ndinakhalako woda bwa pakati pao masiku asanu ndi
awiri.

Mlonda wa Israyeli

16Ndipo kunali atatha masiku asanu ndi awiri, mau a Yehova
anandidzera, ndi kuti, 17Wobadwa ndi munthu iwe, ndakuika
ukhale mlonda wa nyumba ya Israyeli, m'mwemo mvera mau
oturuka m'kamwa mwanga, nundicenjezere iwo. 18Ndikanena kwa
woipa, Udzafa ndithu, koma iwe osamcenjeza, wosanena
kumcenjeza woipayo aleke njira yace yoipa, kumsunga ndi moyo,
woipa yemweyo adzafa mu mphulupulu yace; koma mwazi wace

ndidzaufuna pa dzanja lako. 19Koma ukacenjeza woipa, osabwerera iye kuleka coipa cace kapena njira yace yoipa, adzafa mu mphulupulu yace; koma iwe walanditsamoyo wako. 20Momwemonso akabwerera wolungama kuleka cilungamo cace, ndi kucita cosalungama, ndipo ndikamuikira comkhumudwitsa, adzafa; popeza sunamcenjeza, adzafa m'cimo lace, ndi zolungama zace adazicita sizidzakumbukika; koma mwazi wace ndidzaufuna pa dzanja lako. 21Koma ukamcenjeza wolungamayo, kuti asacimwe wolungamayo, ndipo sacimwa, adzakhala ndi moyo ndithu, popeza anacenjezedwa; ndipo iwe walanditsa moyo wako.
22Ndipo dzanja la Yehova linandikhalira komweko, nati kwa ine, Nyamuka, turuka kumka kucidikha, ndipo pomwepo ndidzalankhula ndi iwe. 23Ndipo ndinauka ndi kuturuka kumka kucidikha, ndipo taonani, ulemerero wa Yehova unaimako monga ulemerero uja ndinauona ku mtsinje Kebara, ndipo ndinagwa nkhope pansi. 24Pamenepo unandilowa mzimu ndi kundiimika ndikhale ciriri; ndipo analankhula ndi ine, nanena nane, Muka, katsekedwe m'nyumba mwako. 25Koma iwe wobadwa ndi munthu, taona, adzakuikira iwe zingwe zolimba, nadzakumanga nazo, ndipo sudzaturuka pakati pao; 26ndipo ndidzamamatiritsa lilime lako ku malakalaka ako, kuti ukhale wosanena, wosawakhalira wakuwadzudzula; pakuti iwo ndiwo nyumba yopanduka. 27Koma pamene ndilankhula nawe ndidzatsegula pakamwa pako, nudzanena nao, Atero Yehova Mulungu. Wakumvera amvere, wasafuna kumvera akhale; pakuti iwo ndiwo nyumba yopanduka.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Aneneratu mophiphiritsa za kumangidwa misasa Yerusalemu

1Ndipo iwe wobadwa ndi munthu, dzitengere njerwa, nulike
pamaso pako, nulembepo mudzi, ndiwo Yerusalemu; 2nuuzinge,
nuumangire nsanja zouzinga, nuundire nthumbira, ndi kuumangira
misasa, nuuikire zogumulira pozungulira pace. 3Nudzitengere
ciwaya cacitsulo, ndi kuciika ngati khoma lacitsulo pakati pa iwe
ndi mudziwo; nuulozetsere nkhope yako kuti umangidwire misasa,
ndipo udzamangira misasa. Ici cikhale cizindikilo ca nyumba ya
Israyeli.
4Ndipo iwe ugonere pansi mbali yako ya kumanzere, nuikepo
mphulupulu ya nyumba ya Israyeli; monga mwa kuwerenga kwa
masiku amene udzagonapo udzasenza mphulupulu yao. 5Ndipo Ine
ndakuikira zaka za mphulupulu yao ngati masiku, ndiwo masiku
mazana atatu mphambu makumi asanu ndi anai, kuti usenze
mphulupulu ya nyumba ya Israyeli. 6Ndipo utatsiriza awa,
ugonerenso mbali yako ya kumanja, ndi kusenza mphulupulu ya
nyumba ya Yuda; ndakuikira masiku makumi anai, kuliyesa tsiku
limodzi ngati caka cimodzi. 7Ndipo ulozetse nkhope yako
kuzingidwa kwace kwa Yerusalemu, ndi dzanja lako losapfundika,
nuunenere. 8Ndipo taona ndidzakumanga ndi zingwe zolimba kuti
usakunkhulire, mpaka watsiriza masiku a kuzingidwa
kwako. 9Udzitengerenso tirigu, ndi barele, ndi nyemba, ndi
mphodza, ndi mapira, ndi mawere, nuziike m'mbale imodzi, ndi
kudzipangira mkate nazo; uzidyako monga mwa kuwerenga kwa
masiku udzagonawo pambali pako, ndiwo masiku mazana atatu
mphambu makumi asanu ndi anai. 10Ndipo cakudya cako uzicidya
ciyesedwe masekeli makumi awiri tsiku limodzi; uzidyako tsiku ndi
tsiku pa nthawi yace. 11Uzimwanso madzi monga mwa muyeso,
limodzi la magawo asanu ndi limodzi la hini; uzimwako tsiku ndi
tsiku pa nthawi yace. 12Ndipo uzicidya ngati timikate ta barele, ndi
kutioca pamaso pao ndi zonyansa za munthu. 13Ndipo Yehova
anati, Motero ana a Israyeli adz adya ca kudya cao codetsedwa,
mwa amitundu kumene ndidzawaingitsirako. 14Pamenepo ndinati,
Ha, Ambuye Yehova! taonani, moyo wanga sunadetsedwa, pakuti
ciyambire ubwana wanga mpaka tsopano sindinadye cinthu cakufa
cokha, kapena cogwidwa ndi cirombo; simunalowanso m'kamwa
mwanga nyama yonyansa. 15Ndipo anati kwa ine, Taona
ndakuninkha ndowe ya ng'ombe m'malo mwa zonyansa za
munthu, uoce mkate wako pamenepo. 16Nanenanso nane,
Wobadwa ndi munthu iwe, taona, ndidzatyola mcirikizo, ndiwo
cakudya, m'Yerusalemu; ndipo adzadya cakudyaco monga mwa
muyeso, ndi mosamalira, nadzamwa madzi monga mwa muyeso,

ndi kudabwa; 17kuti asowe cakudya ndi madzi, nasumwesumwe,
naondetse mu mphulupulu zao.

©The Bible Society of Malawi, 1992

1Ndipo iwe wobadwa ndi munthu, udzitengere mpeni wakuthwa,
ndiwo lumo la wometa, udzitengere ndi kulipititsa pamutu pako ndi
pa ndebvu zako; nudzitengere muyeso kuyesa nao, ndi kugawa
tsitsilo. 2Limodzi la magawo ace atatu utenthe ndi moto pakati pa
mudzi pakutha masiku a kuzingidwa mudzi, nutenge gawo lina ndi
kukwapula-kwapula ndi lupanga pozungulira pace, nuwaze
kumphepo gawo lotsala; pakuti ndidzasolola lupanga
lakuwatsata. 3Utengekonso owerengeka ndi kuwamanga m'mkawo
wa maraya ako. 4Nutengekonso pa amenewa ndi kuwaponya pakati
pa moto, ndi kuwatentha m'moto; kucokera kumeneko udzaturuka
moto pa nyumba yonse ya Israyeli.

Aneneratu za kupasuka kwa Yerusalemu

5Atero Yehova Mulungu, Uwu ndi Yerusalemu ndinauika pakati pa
amitundu, ndi pozungulira pace pali maiko. 6Koma anakaniza
maweruzo anga ndi kucita zoipa koposa amitundu, nakaniza
malemba anga koposa maiko akuuzungulira; pakuti anataya
maweruzo anga, ndi malemba anga, sanayendamo. 7Cifukwa cace
atero Ambuye Yehova, Popeza kupokosera kwanu kwaposa kwa
amitundu akukuzingani, ndipo simunayenda m'malemba anga,
kapena kucita maweruzo anga, ngakhale maweruzo a amitundu
akukuzingani simunawacita; 8cifukwa cace atero Ambuye Yehova,
Taona ndidzatsutsana nawe Inedi, ndi kucita maweruzo pakati pako
pamaso pa amitundu. 9Ndipo ndidzacita mwa iwe cimene
sindinacicita ndi kale lonse, ndi kusadzacitanso momwemo,
cifukwa ca zonyansa zako zonse. 10Cifukwa cace atate adzadya
ana pakati pako, ndi ana adzadya atate ao; ndipo ndidzacita
maweruzo mwa iwe, ndi akutsala onse ndidzawabalalitsa ku
mphepo zonse. 11M'mwemo, Pali Ine, ati Ambuye Yehova, popeza
wadetsa malo anga opatulika ndi zonyansa zako zonse ndi zoipsa
zako zonse, ndidzakucepsa; diso langa silidzalekerera, ndi Inenso
sindidzacita cifundo. 12Limodzi la magawo atatu la iwe lidzafa ndi
mliri, nilidzatha ndi njala pakati pa iwe; ndi limodzi lidzagwa ndi
lupanga pozinga pako; ndi limodzi ndidzalibalalikitsa ku mphepo
zonse, ndi kuwasololera lupanga lakuwatsata. 13Motero mkwiyo
wanga udzakwaniridwa, ndipo ndidzakhutitsa ukali wanga pa iwo,
ndi kudzitonthoza; ndipo adzadziwa kuti Ine Yehova ndinanena
m'cangu canga, pokwaniridwa nao ukali wanga. 14Ndidzakuikanso
ukhale bwinja ndi cotonza pakati pa amitundu akukuzinga, pamaso
pa onse akupitirirapo. 15Momwemo cidzakhala cotonza ndi
mnyozo, cilangizo ndi codabwiza kwa amitundu akukuzinga,
pamene ndikucitira maweruzo mu mkwiyo ndi ukali ndi
madzudzulo aukali; Ine Yehovandanena. 16Pakuwatumizira Ine
mibvi yoipa ya njala yakuononga, imene ndidzatumiza

kukuonongani, pamenepo ndidzakukuzirani njala, ndi kukutyolerani mcirikizo, ndiwo cakudya. 17Inde ndidzakutumizirani njala ndi zirombo, ndipo zidzakusowetsa ana ako; ndi mliri ndi mwazi zidzakugwera; ndidzakufikitsiranso lupanga; Ine Yehova ndacinena.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Aneneratu motsutsa mapiri a Israyeli

1Ndipo mau a Yehova anandidzera, kuti, 2Wobadwa ndi munthu
iwe, lozetsa nkhope yako ku mapiri a Israyeli, uwanenere, 3nunene,
Mapiri a Israyeli inu, tamverani mau a Yehova Mulungu: Atero
Yehova Mulungu kwa mapiri ndi zitunda, kwa mitsinje ndi zigwa,
Taonani, Ine ndikufikitsirani lupanga, ndipo ndidzaononga misanje
yanu. 4Ndi maguwa anu a nsembe adzakhala opasuka, ndi
zoimiritsa zanu zadzuwa zidzasweka; ndipo ndidzagwetsa ophedwa
anu pamaso pa mafano anu. 5Ndipo ndidzaika mitembo ya ana a
Israyeli pamaso pa mafano anu, ndi kumwaza mafupa anu
mozungulira maguwa anu a nsembe. 6Pokhala inu ponse midzi
idzapasuka, ndi misanje idzakhala yabwinja; kuti maguwa anu a
nsembe akhale opasuka ndi mabwinja, ndi mafano anu asweke
nalekeke, ndi zoimiritsa zanu zadzuwa zilikhidwe, ndi nchito zanu
zifafanizidwe. 7Ndi ophedwa adzagwa pakati panu, matero
mudzadziwa kuti Ine ndine Yehova. 8Koma ndidzasiyapo otsala,
popeza mudzakhala nao ena akupulumuka lupanga mwa amitundu
pobalalitsidwa inu m'maiko maiko. 9Pamenepo akupulumuka anu
adzandikumbukila Ine kwa amitundu kumene anatengedwa
ndende, kuti ndasweka ndi mtima wao wacigololo wolekana ndi
Ine, ndi maso ao acigololo akutsata mafano ao; ndipo iwo
adzakhala onyansa pamaso pao pa iwo eni, cifukwa ca zoipa
anazicita m'zonyansa zao zonse. 10Ndipo adzadziwa kuti Ine ndine
Yehova, sindinanena cabe kuti ndidzawacitira coipa ici.
11Atero Yehova Mulungu, Omba manja ako, ponda ndi phazi lako,
nuti, Kalanga ine, cifukwa ca zonyansa zoipa zonse za nyumba ya
Israyeli; pakuti adzagwa ndi lupanga, ndi njala, ndi mliri. 12Wokhala
kutali adzafa ndi mliri, wakhala pafupi adzagwa ndi lupanga; koma
wotsala ndi kuzingidwa adzafa ndi njala; momwemo
ndidzawakwaniritsira ukali wanga, 13Ndipo mudzadziwa kuti Ine
ndine Yehova, pokhala ophedwa ao pakati pa mafano ao, pozinga
maguwa ao a nsembe, pa zitunda zonse zazitali, pamwamba pa
mapiri onse, ndi patsinde pa mitengo yogudira yonse, ndi patsinde
pa thundu ali yense wagudugudu, pomwe adapereka zonunkhira
zokoma kwa mafano ao onse. 14Ndipo ndidzawatambasulira dzanja
langa, ndi kulisandutsa dziko bwinja ndi lopasuka, koposa cipululu
ca ku Dibla mokhalamo iwo monse; ndipo adzadziwa kuti Ine ndine
Yehova.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Kutha kwace kwa dziko la Israyeli

1Ndipo mau a Yehova anandidzera, akuti, 2Ndipo iwe wobadwa ndi munthu, atero Ambuye Yehova kwa dziko la Israyeli, Kwatha; kwafika kutha kwace pa ngondya zinai za dziko. 3Tsopano kwakudzera kutha kwako, ndipo ndidzakutumizira mkwiyo wanga, ndi kukuweruza monga mwa njira zako, ndipo ndidzakubwezera zonyansa zako zanse. 4Ndipo diso langa silidzakulekerera, sindidzacita cifundo, koma ndidzakubwezera njira zako, ndi zonyansa zako zidzakhala pakati pako; ndipo mudzadziwa kuti Ine ndine Yehova.

5Atero Yehova Mulungu, Coipa, coipa ca pa cokha, taona cirinkudza. 6Kutha kwafika, kwafika kutha, kwakugalamukira, taona kwafika. 7Tsoka lako lakufikira, nzika iwe, yafika nthawi, tsiku liri pafupi, ndilo laphokoso, si lakupfuula mokondwera kumapiri, 8Katsala kamphindi, ndipo ndidzakutsanulira ukali wanga, ndi kukukwaniritsira mkwiyo wanga, ndi kukuweruza monga mwa njira zako, ndipo ndidzakubwezera zonyansa zako zonse. 9Ndipo diso langa silidzalekerera, wosacita cifundo Ine, ndidzakubwezera monga mwa njira zako, ndi zonyansa zako zidzakhala pakati pako; ndipo mudzadziwa kuti Ine ndine Yehova wakukantha. 10Taona, tsikuli, taona, lafika; tsoka lako laturuka, ndodo yaphuka mphundu za maluwa, kudzitama kwaphuka. 11Ciwawa cauka cikhale ndodo ya coipa; sadzawatsalira ndi mmodzi yense, kapena wa unyinji wao, kapena wa cuma cao; sipadzakhalanso kuwalira maliro. 12Yafika nthawi, layandikira tsikulo, wogula asakondwere, ndi wogulitsa asamve cisoni; pakuti mkwiyo ukhalira unyinji wao wense. 13Pakuti wogulitsa sadzabwera ku cogulitsaco, cinkana akali ndi moyo, popeza masomphenyawo akunena unyinji wace wonse sadzapita pacabe, ndipo palibe mmodzi adzalimbitsa moyo wace m'mphulupulu yace. 14Aomba lipenga, nakonzeratu zonse, koma palibe womuka kunkhondo; pakuti mkwiyo wanga ukhalira unyinji wace wonse. 15Kunja kuli lupanga, ndi m'katimo muli mliri ndi njala; wokhala kuthenso adzafa ndi lupanga, ndi wokhala m'mudziyo njala ndi mliri zidzamutha. 16Ndipo akupulumuka mwa iwo adzapulumuka, koma adzakhala kumapiri ngati njiwa za kuzigwa, onse akubuula, ali yense m'mphulupulu zace. 17Manja onse adzalenda, ndi maondo onse adzaweyeseka ngati madzi. 18Ndipo adzadzimangira m'cuuno ndi ziguduli, ndi zoopsetsa zidzawaphimba, ndi nkhope zonse zidzacita manyazi, ndi mitu yao yonse idzacita dazi. 19Adzataya siliva wao kumakwalala, nadzayesa golidi wao cinthu codetsedwa; siliva wao ndi golidi wao sadzakhoza kuwalanditsa tsiku la mkwiyo wa Yehova, sadzakwaniritsa moyo wao, kapena kudzaza matumbo

ao; pakuti izi ndi cokhumudwitsa ca mphulupulu zao. 20Ndipo
cokometsera cace cokongola anaciyesa codzikuza naco, napanga
naco mafanizo ao onyansa, ndi zonyansa zao zina; cifukwa cace
ndinapatsa ici cikhale cowadetsa. 21Ndipo ndidzacipereka m'dzanja
la alendo cikhale colandika, ndi kwa oipa a m'dziko cikhale
cofunkha; ndipo adzaciipsa. 22Ndipo nkhope yanga
idzawayang'anira kumbali, ndipo iwo adzadetsa pobisika panga,
nadzalowamo acifwamba, nadzamudetsa. 23Sula unyolo, popeza
dziko ladzala ndi mirandu yamwazi, ndi mudzi wadzala ndi
ciwawa. 24Cifukwa cace ndidzabwera nao amitundu oipitsitsa,
ndipo iwo adzalandira nyumba zao ngati colowa, ndidzaleketsanso
kudzikuza kwa amphamvu, kuti adetsedwe malo ao
opatulika. 25Cionongeko cirinkudza, adzafunafuna mtendere, koma
palibe. 26Lidzafika tsoka lotsatana-tsatana, kudzakhalanso mbiri
yotsatana-tsatana, ndipo adzafunafuna masomphenya a mneneri,
koma malamulo adzatayikira wansembe, uphungu ndi kutayikira
akulu. 27Mfumu idzalira maliro, ndi kalonga adzabvala cipasuko,
ndi manja a anthu a m'dziko adzanjenjemera, Ndidzawacitira
monga mwa njira zao, ndi kuwaweruza monga mwa maweruzo ao;
ndipo adzadziwa kuti Ine ndine Yehova.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masomphenya a zoipitsitsa za m'Kacisi

1Ndipo kunali caka cacisanu ndi cimodzi, mwezi wacisanu ndi cimodzi, tsiku lacisanu la mweziwo, pokhala ine m'nyumba mwanga, akulu a Yuda omwe analikukhala pamaso panga, dzanja la Yehova Mulungu linandigwera komweko. 2Ndipo ndinapenya, ndipo taonani, cifaniziro ca maonekedwe a moto; kuyambira maonekedwe a m'cuuno mwace ndi kunsi kwace, moto; ndi kuyambira m'cuuno mwace ndi kumwamba kwace, monga maonekedwe a ceza, ngan citsulo cakupsa. 3Ndipo anatambasula conga dzanja, nandigwira tsitsi la pamutu panga; ndipo mzimu unandilengetsa pakati pa dziko ndi thambo, numuka nane m'masomphenya a Mulungu ku Yerusalemu, ku citseko ca cipata ca bwalo la m'katimo loloza kumpoto, kumene kunali mpando wa fano la nsanje locititsa nsanje. 4Ndipo taonani, pomwepo panali ulemerero wa Mulungu wa Israyeli, monga mwa maonekedwe ndinawaona ku cidikha cija. 5Pamenepo ananena ndi ine, Wobadwa ndi munthu iwe, kweza maso ako ku njira yoloza kumpoto. Ndipo ndinakweza maso anga ku njira yoloza kumpoto, ndipo taonani, kumpoto kwa cipata ca guwa la nsembe fano ili la nsanje polowera pace. 6Ndipo anati kwa ine, Wobadwa ndi munthu iwe, uona kodi izi alikuzicita? zonyansa zazikulu nyumba ya Israyeli irikuzicita kuno, kuti ndicoke kutali kwa malo anga opatulika? Koma udzaonanso zonyansa zina zoposa. 7Ndipo anadza nane ku cipata ca kubwalo, ndipo popenya ine, taonani, pobooka palinga. 8Pamenepo anati kwa ine, Wobadwa ndi munthu iwe, booletsa kulinga; ndipo ndita booletsa palinga, ndinaona khomo. 9Ndipo anati kwa ine, Lowa, kapenye zonyansa zoipa alikuzicita komweko. 10M'mwemo ndinalowa ndi kupenya, ndipo taonani, maonekedwe ali onse a zokwawa, ndi zirombo zonyansa, ndi mafano onse a nyumba ya Israyeli, zolembedwa pakhoma pozungulira ponse. 11Ndipo pamaso pao panaima amuna makumi asanu ndi awiri a akulu a nyumba ya Israyeli, ndi pakati pao panaima Jazaniya mwana wa Safana munthu ali yense ndi mbale yace ya zofukiza m'dzanja lace; ndi pfungo lace la mtambo wa zonunkhira linakwera. 12Pamenepo anati kwa ine, Wobadwa ndi munthu iwe, wapenya kodi cocita akulu a nyumba ya Israyeli mumdima, ali yense m'cipinda cace ca zifanizo? pakuti ati, Yehova satipenya, Yehova wataya dziko. 13Anatinso kwa ine, Udzaonanso zonyansa zazikuru zina azicita. 14Pamenepo anadza nane ku citseko ca cipata ca nyumba ya Yehova coloza kumpoto; ndipo taonani, apo panakhala akazi akulirira Tainuzi. 15Ndipo anati kwa ine, Waciona ici, wobadwa ndi munthu iwe? udzaonanso zonyansa zazikuru zoposa izi. 16Ndipo anadza nane ku bwalo lam'kati la

nyumba ya Yehova, ndipo taonani, pa khomo la Kacisi wa Yehova, pakati pa khonde lace ndi guwa la nsembe, panali amuna ngati makumi awiri mphambu asanu akufulatira, ku Kacisi wa Yehova, ndi kuyang'ana kum'mawa; napembedza dzuwa kum'mawa. 17Ndipo anati kwa ine, Waciona ici, wobadwa ndi munthu iwe? Cinthu copepuka ici kodi ndi nyumba ya Yuda, kuti acite zonyansa azicita kunozi? pakuti anadzaza dziko ndi ciwawa, nabwereranso kuutsa mkwiyo wanga, ndipo taonani, aika nthambi kumphuno kwao. 18Cifukwa cace Inenso ndidzacita mwaukali; diso langa silidzalekerera, osawacitira cifundo Ine; ndipo cinkana apfuula m'makutu mwanga ndi mau akulu, koma sindidzawamvera ine.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Malango apa ocimwa

1Pamenepo Iye anapfuula m'makutu mwanga ndi mau akuru, ndi
kuti, Asendere oyang'anira mudzi, ali yense ndi cida cace
coonongera m'dzanja lace. 2Ndipo taonani, anadza amuna asanu
ndi mmodzi, odzera njira ya cipata ca kumtunda coloza kumpoto,
ali yense ndi cida cace cophera m'dzanja lace; ndi munthu mmodzi
pakati pao wobvala bafuta, ndi zolembera nazo m'cuuno mwace.
Ndipo analowa, naima m'mphepete mwa guwa la nsembe
lamkuwa. 3Ndipo ulemerero wa Mulungu wa Israyeli unakwera
kucoka pakerubi, pamene unakhalira kumka ku ciunda ca nyumba,
naitana munthu wobvala bafutayo wokhala ndi zolembera nazo
m'cuuno mwace. 4Ndipo Yehova ananena naye, Pita pakati pa
mudzi, pakati pa Yerusalemu, nulembe cizindikilo pa mphumi zao
za anthu akuusa moyo ndi kulira cifukwa ca zonyansa zonse
zicitidwa pakati pace. 5Nati kwa enawo, nditikumva ine, Pitani
pakati pa mudzi kumtsata iye, ndi kukantha; maso anu
asalekererere, musacite cifundo; 6iphanitu nkhalamba, mnyamata
ndi namwali, makanda, ndi akazi; koma musayandikira munthu ali
yense ali naco cizindikilo, ndipo muyambe pa malo anga opatulika,
Pamenepo anayamba ndi akuluwo anali pakhomo pa
nyumba. 7Nati kwa iwo, Muipse nyumbayi ndi kudzaza mabwalo
ndi ophedwa, mukani. Ndipo anaturuka, nakantha
m'mudzimo. 8Ndipo kunali, alimkukantha iwo, nditatsala ine,
ndinagwa nkhope yanga pansi, ndi kupfuula, ndi kuti, Kalanga ine.
Ambuye Mulungu! kodi mudzaononga otsala onse a Israyeli
pakutsanulira ukali wanu pa Yerusalemu? 9Pamenepo ananena
nane, Mphulupulu ya nyumba ya Israyeli ndi Yuda ndi yaikurukuru
ndithu, ndi dziko ladzala ndi mwazi, ndi mudziwo wadzala ndi
kukhotetsa mirandu; pakuti ati, Yehova wataya dziko, Yehova
sapenya. 10Ndipo Inenso diso langa silidzalekerera, wosacita
cifundo Ine, koma ndidzawabwezera njira yao pamtu pao. 11Ndipo
taonani, munthu wobvala bafutayo, wokhala ndi zolembera nazo
m'cuuno mwace, anabweza mau, ndi kuti, Ndacita monga
munandilamulira ine.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masomphenya a akerubi

1Ndipo ndinapenya, ndipo taonani, ku thambo lokhala pamwamba
pa mitu ya akerubi kudaoneka ngati mwala wasafiro, ngati
maonekedwe a cifaniziro ca mpando wacifumu pamwamba
pao. 2Ndipo Yehova analankhula ndi munthu wobvala bafuta, nati,
Lowa pakati pa njingazi pansi pa kerubi, nudzaze manja ako
makara a moto ocokera pakati pa akerubi, nuwamwaze
pamwamba pa mudzi. Nalowa, ndiri cipenyere ine. 3Tsono akerubi
anaima ku dzanja lamanja la nyumba polowa munthuyo, ndi
mtambo unadzara bwalo la m'kati. 4Ndipo ulemerero wa Yehova
unakwera kucokera kukerubi kumka ku ciundo ca nyumba; ndi
nyumba inadzala nao mtambo, ndi bwalo linadzala ndi ceza ca
ulemerero wa Yehova. 5Ndipo mkokomo wa mapiko a akerubi
unamveka mpaka bwalo lakunja, ngati mau a Mulungu
Wamphamvuyonse, pakunena Iye. 6Ndipo kunali pomlamulira
munthu wobvala bafutayo, ndi kuti, Para moto pakati pa njingazi
ndi pakati pa akerubi; iye analowa, naima m'mbali mwa
njinga. 7Pamenepo kerubi wina anatambasula dzanja lace pakati
pa akerubi ku moto uli pakati pa akerubi, naparako, nauika
m'manja mwa iye wobvala bafuta, ndiye naulandita,
naturuka. 8Ndipo panaoneka pa akerubi conga dzanja la munthu
pansi pa mapiko ao. 9Pamenepo ndinapenya, ndipo taonani, njinga
zinai m'mbali mwa akerubi, njinga imodzi m'mbali mwa kerubi
mmodzi, ndi njinga yina m'mbali mwa kerubi wina, ndi
maonekedwe a njingazi ananga mawalidwe a berulo. 10Ndipo
maonekedwe ace, zonse zinai zinafanana, ngati njinga ziwiri
zopingasitsana, 11Pakuyenda akerubi anayenda ku mbali zao zinai,
sanatembenuka poyenda; koma komwe udalozako mutu
anatsatako, sanatembenuka poyenda. 12Ndipo thupi lao lonse, ndi
misana yao, ndi manja ao, ndi mapiko ao, ndi njinga zomwe,
zinadzala ndi maso pozungulira pao, zingakhale njingazi anai aja
anali nazo. 13Kunena za njingazi, wina anazipfuulira, ndiri cimvere
ine, Kunkhulirani. 14Ndipo ali yense anali nazo nkhope zinai,
nkhope yoyamba ndiyo nkhope ya kerubi, ndi nkhope yaciwiri
ndiyo nkhope ya munthu, ndi yacitatu ndiyo nkhope ya mkango,
ndi yacinai ndiyo nkhope ya ciombankhanga. 15Pamenepo akerubi
anakwera, ndizo zamoyo zija ndinaziona kumtsinje Kebara. 16Ndipo
pakuyenda akerubi, njinga zinayenda pambali pao, ndi
pakutambasula mapiko ao akerubiwo kuuluka padziko, njingazi
sizinatembenuka pambali pao. 17Pakuima iwo zinaima izi, ndi
pakukwera iwo izi zinakwera pamodzi nao; pakuti mzimu wa
zamoyozo unali mwa izo. 18Ndipo ulemerero wa Yehova unacoka
pa ciundo ca nyumba, nuima pamwamba pa akeruibi. 19Ndipo

akerubi anatambasula mapiko ao, nauluka padziko, ndiri cipenyere, pakucoka iwo ndi njingazi pa mbali pao; ndipo anaima pa citseko ca cipata ca kum'mawa ca nyumba ya Yehova, ndi ulemerero wa Mulungu wa Israyeli unali pamwamba pao. 20Awa ndi zamoyozo ndinaziona pansi pa Mulungu wa Israyeli kumtsinje Kebara, ndipo ndinadziwa kuti ndiwo akerubi. 21Yense anali nazo nkhope zinai, ndi yense mapiko anai, ndi cifaniziro ca manja a munthu pansi pa mapiko ao. 22Ndi cifaniziro ca nkhope zao ndico nkhope zomwezo ndinaziona kumtsinje Kebara, maonekedwe ao ndi iwo eni; ali yense anayenda, nalunjika m'tsogolo.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Ciweruzo ca Mulungu pa mafumu a Ayuda

1Pamenepo unandikweza mzimu, nudza nane ku cipata ca
kum'mawa ca nyumba ya Yehova coloza kum'mawa; ndipo taonani,
pa citseko ca cipata amuna makumi awiri mphambu asanu; ndipo
ndinaona pakati pao Yazaniya mwana wa Azuri ndi Pelatiya mwana
wa Benaya, akalonga a anthu. 2Ndipo anati kwa ine, Wobadwa ndi
munthu iwe, awa ndi anthu olingirira za mphulupulu, ndi kupangira
uphungu woipa m'mudzi muno; 3ndiwo akuti, siinafike nyengo
yakumanga nyumba; mudzi uwu ndi mphika, ife ndife
nyama. 4Cifukwa cace uwanenere, neneratu, wobadwa ndi munthu
iwe. 5Pamenepo mzimu wa Yehova unandigwera, ndipo ananti kwa
ine, Nena, Atero Yehova, Mwatero nyumba ya Israyeli, pakuti
ndidziwa zimene zimalowa m'mtima mwanu. 6Mwacurukitsa
ophedwa anu m'mudzi muno, mwadzazanso makwalala ace ndi
ophedwawo. 7Cifukwa cace atero Yehova Mulungu, Ophedwa anu
munawaika m'kati mwace, iwo ndiwo nyama imene, ndi mudzi uwu
ndiwo mphika; koma inu mudzaturutsidwa m'kati mwace. 8Mwaopa
lupanga, tsono ndidzakufikitsirani lupanga, ati Yehova
Mulungu. 9Ndipo ndidzakuturutsani m'kati mwace, ndi
kukuperekani m'manja a alendo, ndi kucita maweruzo pakati
panu. 10Mudzagwa ndi lupanga, ndidzakuweruzirani ku malire a
Israyeli; ndipo mudzadziwa kuti Ine ndine Yehova. 11Mudzi uno
sudzakhala mphika wanu, ndi inu simudzakhala nyama m'kati
mwace, ndidzakuweruzirani ku malire a Israyeli; 12ndipo
mudzadziwa kuti Ine ndine Yehova, pakuti simunayenda
m'malemba anga, kapena kucita maweruzo anga, koma mwacita
monga mwa maweruzo a amitundu okhala pozungulira
panu. 13Ndipo kunali, pakunenera ine, anamwalira Pelatiya mwana
wa Benaya. Pamenepo ndinagwa nkhope yanga pansi, ndi kupfuula
ndi mau akuru, ndi kuti, Kalanga ine, Yehova Mulungu!
mudzatsiriza kodi otsala a Israyeli?
14Ndipo mau a Yehova anandidzera kuti, 15Wobadwa ndi munthu
iwe, abale ako, inde abale ako amuna a cibale cako, ndi nyumba
yonse ya Israyeli, yonseyi ndiwo amene okhala m'Yerusalemu
ananena nao, Muzikhala kutali kwa Yehova; dziko ili lapatsidwa kwa
ife, likhale colowa cathu; 16cifukwa cace uziti, Atero Yehova
Mulungu, Ngakhale ndawacotsa kutali mwa amitundu, ngakhalenso
ndawabalalikitsa m'maiko, koma ndidzawakhalira malo opatulika
kanthawi ku maiko adafikako. 17Cifukwa cace uziti, Atero Yehova
Mulungu, Ndidzakumemezani ku mitundu ya anthu, ndi
kukusonkhanitsani mucoke m'maiko m'mene munabalalikiramo,
ndipo ndidzakuninkhani dziko la Israyeli. 18Ndipo adzafikako,
nadzacotsako zonyansa zace zonse, ndi zace zonse

zakuipitsamo. 19Ndipo ndidzawapatsa mtima umodzi, ndi kuika
mzimu watsopano m'kati mwao; ndipo ndidzawacotsera mtima
wamwala m'thupi mwao, ndi kuwapatsa mtima wamnofu; 20kuti
ayende m'malemba anga, ndi kusunga maweruzo anga, ndi
kuwacita; ndipo adzakhala anthu anga, ndi Ine ndidzakhala
Mulungu wao. 21Koma iwo amene mtima wao unatsata mtima wa
zonyansa zao, ndi zoipitsitsa zao, ndidzawabwezera njira yao
pamtu pao, ati Yehova Mulungu. 22Pamenepo akerubi
anatambasula mapiko ao, ndi njinga zinali pa mbali pao; ndi
ulemerero wa Mulungu wa Israyeli unali pamwamba pao. 23Ndipo
ulemerero wa Yehova unakwera kucoka pakati pa mudzi, nuima pa
phiri la kum'mawa kwa mudzi. 24Ndipo mzimu unandikweza, nufika
nane m'masomphenya mwa mzimu wa Mulungu ku dziko la
Akasidi, kwa andendewo. M'mwemo masomphenya ndidawaona
anandicokera, nakwera. 25Pamenepo ndinanena ndi andendewo
zonse zija adandionetsa Yehova.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Khoma labooledwa lofanizira ukapolo ndi ubalaliko wao

1Mau a Yehova anandidzeranso, ndi kuti, 2Wobadwa ndi munthu
iwe, ukhala pakati pa nyumba yampanduko, yokhala nao maso
akuonera, koma osaona; ndi makutu akumvera, koma osamva;
pakuti iwo ndiwo nyumba yampanduko. 3Potero wobadwa ndi
munthu iwe, udzikonzeretu akatundu a pa ulendo wa kundende,
nucoke usana pamaso pao, ucoke pakhala iwepo kumka malo ena
pamaso pao; kapena adzacizindikira, angakhalendiwo
nyumbayopanduka. 4Uziturutsa akatundu ako usana pamaso pao,
ngati a pa ulendo wa kundende; ndipo madzulo uzituruka wekha
pamaso pao, monga amaturuka olowa kundende. 5Udziboolere
khoma pamaso pao, nuwaturutsire akatundu pamenepo, 6Pamaso
pao uwasenze paphewa pako, ndi kuwaturutsa kuli mdima,
nuphimbe nkhope yako kuti usapenye dziko; popeza ndakuika
cizindikilo ca nyumba ya Israyeli. 7Ndipo ndinacita monga momwe
anandilamulira, ndinaturutsa akatundu anga usana, ngati a pa
ulendo wa kundende, ndi madzulo ndinaboola pakhoma ndi dzanja
langa, ndinawaturutsa pali mdima, ndi kuwasenza paphewa panga
pamaso: pao. 8Ndipo m'mawa mau a Yehova anandidzera, ndi
kuti, 9Wobadwa ndi munthu iwe, kodi nyumba ya Israyeli, nyumba
yampanduko, siinati kwa iwe. Ucitanji? 10Unene nao, Atero Ambuye
Yehova, Katundu uyu anena za kalonga wa m'Yerusalemu, ndi
nyumba yonse ya Israyeli yokhala pakati pao. 11Uziti, Ine ndine
cizindikilo canu, monga ndacita ine momwemo kudzacitidwa nao;
adzacotsedwa kumka kundende. 12Kalongayo ali pakati pao
adzasenza paphewa pace mumdima, nadzaturuka; adzaboola
palinga, nadzaturutsapo; adzaphimba nkhope yace kuti asapenye
dziko ndi maso ace. 13Ndidzamphimba ndi ukonde wanga,
nadzakodwa iye mu msampha wanga; ndipo ndidzafika naye ku
Babulo, ku dziko la Akasidi; sadzaliona, cinkana adzafako. 14Ndipo
onse omzinga kumthandiza, ndi magulu ace onse, ndidzawamwaza
ku mphepo zonse, ndidzawasololeranso lupanga
lakuwatsata. 15Motero adzadziwa kuti Ine ndine Yehova,
pakuwamwaza Ine mwa amitundu, ndi kuwabalalitsa
m'maiko. 16Koma ndidzawasiya owerengeka apulumuke lupanga,
ndi njala, ndi mliri, kuti afotokoze zonyansa zao kwa amitundu
kumene afikako; ndipo adzadziwa kuti Ine ndine Yehova.
17Anandidzeranso mau a Mulungu, akuti, 18Wobadwa ndi munthu
iwe, udye mkate wako ndi kunthunthumira, ndi kumwa madzi ako
ndi kunjenjemera, ndi kutenga nkhawa; 19nunene kwa anthu a
m'dziko, Atero Yehova Mulungu za iwo okhala m'Yerusalemu, ndi za
dziko la Israyeli, Adzadya mkate wao ndi nkhawa, ndi kumwa
madzi ao ndi kusumwa; pakuti dziko lao lidzakhala lacipululu,

kuleka kudzala kwace cifukwa ca ciwawa ca onse okhalamo. 20Ndi
midzi yokhalamo anthu idzapasuka, ndi dziko lidzakhala labwinja;
ndipo mudzadziwa kuti Ine ndine Yehova.

Aneneratu kutsutsa aneneri onama

21Ndipo anandidzera mau a Yehova, akuti, 22Wobadwa ndi munthu
iwe, ngwotani mwambi umene muli nao m'dziko la Israyeli, wakuti,
Masiku acuruka, ndi masomphenya ali onse apita
pacabe? 23Cifukwa cace unene nao, Atero Yehova Mulungu,
Ndidzaleketsa mwambi uwu, ndipo sadzauchulanso mwambi
m'Israyeli; koma unene nao, Masiku ayandikira, nadzacitika
masomphenya ali onse. 24Pakuti sikudzakhalanso masomphenya
acabe, kapena ula wosyasyalika m'nyumba ya Israyeli. 25Pakuti Ine
ndine Yehova, ndidzanena, ndi mau ndidzanenawo adzacitika,
osazengerezekanso; pakuti m'masiku anu, nyumba yopanduka inu,
ndidzanena mau ndi kuwacita, ati Yehova Mulungu.
26Anandidzeranso mau a Yehova, akuti, 27Wobadwa ndi munthu
iwe, taona, iwo a nyumba ya Israyeli akuti, masomphenya awaona
ndiwo a masiku ambiri: ndipo anenera za nthawi ziri
kutali, 28Cifukwa cace uziti nao, Atero Ambuye Yehova, Palibe
amodzi a mau anga adzazengerezekanso; koma mau
ndidzanenawo adzacitika, ati Ambuye Yehova.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Ezekieli 13

1Ndipo mau a Yehova anandidzera ine, akuti, 2Wobadwa ndi munthu iwe, Unenere za aneneri a Israyeli onenerawo, nuziti nao onenera za m'mtima mwao mwao, Tamverani mau a Yehova. 3Atero Ambuye Yehova, Tsoka aneneri opusawo akutsata mzimu wao wao, cinkana sanaona kanthu. 4Aneneri ako, Israyeli, akhala ngati nkhandwe m'mapululu. 5Simunakwera kuima mopasuka, kapena kumanganso linga la nyumba ya Israyeli, kuima kunkhondo tsiku la Yehova. 6Iwo aona zopanda pace, ndi phenda labodza amene anena, Atero Yehova; koma Yehova sanawatuma, nayembekezetsa anthu kuti mauwo adzakhazikika. 7Simunaona masomphenya opanda pace kodi? simunanena ula wabodza kodi? pakunena inu, Atero Yehova; cinkana sindinanena?

8Cifukwa cace atero Ambuye Yehova, Popeza mwanena zopanda pace, ndi kuona mabodza, cifukwa cace taonani, ndikhala Ine wotsutsana nanu, ati Ambuye Yehova. 9Ndi dzanja langa lidzakhala lotsutsana nao aneneri akuona zopanda pace, ndi kupenda za bodza; sadzakhala mu msonkhano wa anthu anga, kapena kulembedwa m'buku lolembedwamo nyumba ya Israyeli, kapena kulowa m'dziko la Israyeli; ndipo mudzadziwa kuti Ine ndine Ambuye Yehova, 10Popeza, inde popeza asokeretsa anthu anga, ndi kuti, Mtendere, pokhala palibe mtendere; ndipo anthu akamanga linga, aneneriwo alimata ndi dothi losapondeka; 11uziti nao olimata ndi dothi losapondeka, kuti lidzagwa, lidzabvumbidwa ndi mvula yaikuru; ndi inu, matalala akuru, mudzagwa; ndi mkuntho udzalithithimula. 12Ndipo taonani, litagwa linga, sadzanena nanu kodi, Liri kuti dothi munalimata nalo? 13Cifukwa cace atero Ambuye Yehova, Ndidzalithithimula ndi mkuntho m'ukali wanga; ndipo lidzabvumbidwa ndi mvula yaikuru mu mkwiyo wanga, ndi matalala akuru adzalitha m'ukali wanga. 14M'mwemo ndidzagumula linga munalimata ndi dothi losapondeka, ndi kuligwetsa pansi; kuti maziko ace agadabuke, ndipo lidzagwa; ndi inu mudzathedwa pakati pace; ndipo mudzadziwa kuti Ine ndine Yehova. 15M'mwemo ndidzakwaniritsa ukali wanga pa lingalo, ndi pa iwo analimata ndi dothi losapondeka, ndipo ndidzati kwa inu, Lingalo palibe, ndi olimata palibe, 16ndiwo aneneri a Israyeli akunenera za Yerusalemu, nauonera masomphenya a mtendere, pamene palibe mtendere, ati Ambuye Yehova.

Mau akutsutsa aneneri akazi onama

17Ndipo iwe wobadwa ndi munthu, uziika nkhope yako itsutsane nao ana akazi a anthu ako, akunenera za m'mtima mwao, nunenere cowatsutsa, 18nuziti, Atero Ambuye Yehova, Tsoka akazi osoka zophimbira mfundo zonse za dzanja, ndi iwo okonza zokuta mitu za misinkhu iri yonse, kuti asake miyoyo! Kodi musaka

miyoyo ya anthu anga ndi kudzisungira miyoyo yanu? 19Ndipo
mundidetsa mwa anthu anga kulandirapo barele wodzala manja,
ndi zidutsu za mkate, kuipha miyoyo yosayenera kufa, ndi kusunga
miyoyo yosayenera kukhala ndi moyo, ndi kunena mabodza kwa
anthu anga omvera bodza. 20Cifukwa cace atero Ambuye Yehova,
Taonani, nditsutsana nazo zophimbira zanu, zimene musaka nazo
miyoyo komweko, kululuza; ndipo ndidzazikwatula m'manja
mwanu, ndi kuimasula, ndiyo miyoyo muisaka kululuza. 21Zokuta
mitu zanu zomwe ndidzazing'amba, ndi kulanditsa anthu anga
m'manja mwanu; ndipo sadzakhalanso m'mphamvu mwanu
kusakidwa; ndipo mudzadziwa kuti Ine ndine Yehova. 22Popeza
mwamvetsa cisoni ndi mabodza mtima wa wolungama, amene
sindinamvetsa cisoni Ine, ndi kumlimbitsa manja woipa, kuti
asabwerere kuleka njira yace yoipa, ndi kusungidwa
wamoyo; 23cifukwa cace simudzaonanso zopanda pace, kapena
kupenda; koma ndidzalanditsa anthu anga m'manja mwanu; ndipo
mudzadziwa kuti Ine ndine Yehova.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Cilango ca pa opembedza mafano

1Pamenepo anafika kwa ine akulu ena a Israyeli nakhala pansi
pamaso panga. 2Ndipo anandidzera mau a Yehova,
akuti, 3Wobadwa ndi munthu iwe, anthu awa anautsa mafano ao
mumtima mwao, naimika cokhumudwitsa ca mphulupulu yao
pamaso pao; ndifunsidwe nao konse kodi? 4Cifukwa cace ulankhule
nao, nunene nao, Atero Ambuye Yehova, Ali yense wa nyumba ya
Israyeli wakuutsa mafano ace mumtima mwace, naimika
cokhumudwitsa ca mphulupulu yace pamaso pace, nadza kwa
mneneri, Ine Yehova ndidzamyankhapo monga mwa mafano ace
aunyinji; 5kuti ndigwire nyumba ya Israyeli mumtima mwao;
popeza onsewo asanduka alendo ndi Ine mwa mafano ao. 6Cifukwa
cace uziti kwa nyumba ya Israyeli, Atero Ambuye Yehova, Bwerani,
lekani mafano anu, tembenuzani nkhope zanu kuzisiya zonyansa
zanu zonse. 7Pakuti ali yense wa nyumba ya Israyeli, kapena wa
alendo ogonera m'Israyeli, wodzisiyanitsa kusatsata Ine, nautsa
mafano ace m'mtima mwace, naimika cokhumudwitsa ca
mphulupulu yace pamaso pace, nadzera mneneri kudzifunsira kwa
Ine, Ine Yehova ndidzamyankha ndekha; 8ndipo ndidzaikira munthu
uyu nkhope yanga imtsutse, ndi kumuyesa codabwitsa, ndi
cizindikilo, ndi mwambi, ndi kumsadza pakati pa anthu anga; ndipo
mudzadziwa kuti Ine ndine Yehova. 9Ndipo akaceteka mneneriyo,
nakanena mau, Ine Yehova ndamceta mneneri uja; ndipo
ndidzamtambasulira dzanja langa, ndi kumuononga pakati pa
anthu anga Israyeli. 10Ndipo adzasenza mphulupulu yao,
mphulupulu ya mneneri idzanga mphulupulu ya uja
wamfunsira; 11kuti nyumba ya Israyeli isasocerenso kusatsata Ine,
kapena kudzidetsanso ndi zolakwa zao zonse; koma kuti akhale
anthu anga, ndipo ndikhale Ine Mulungu wao, ati Ambuye Yehova.

Malango a Mulungu ali olungama

12Ndipo anandidzera mau a Yehova akuti, 13Likandicimwira dziko
ndi kucita monyenga, ndipo ndikalitambasulira dzanja langa, ndi
kulityolera mcirikizo wace, ndiwo mkate, ndi kulitumizira njala, ndi
kulidulira munthu ndi nyama, 14cinkana akadakhala m'mwemo
anthu awa atatu, Nowa, Danieli, ndi Yobu, akadapulumutsa moyo
wao wokha mwa cilungamo cao, ati Ambuye Yehova. 15Ndikapititsa
zirombo zoipa pakati pa dziko, nizipulula ana, kuti likhale lacipululu
losapitako munthu cifukwa ca zirombo, 16cinkana anthu omwewo
atatu akadakhala m'mwemo, Pali Ine, ati Ambuye Yehova,
sakadapulumutsa ana amuna kapena akazi; iwo akadapulumuka
okha; koma dziko likadakhala lacipululu. 17Kapena ndikadza pa
dziko ndi lupanga, ndi kuti, Lupanga lipite pakati pa dziko, kuti
ndilidulire munthu ndi nyama; 18cinkana anthu atatuwo

akadakhala m'mwemo, Pali Ine, ati Ambuye Yehova,
sakadapulumutsa ana amuna kapena akazi; koma iwo
akadapulumuka okha. 19Kapena ndikatumizira dzikolo mliri, ndi
kulitsanulira ukali wanga ndi mwazi, kulidulira munthu ndi
nyama; 20cinkana Nowa, Danieli, ndi Yobu, akadakhala m'mwemo,
Pali Ine, ati Ambuye Yehova, sakadapulumutsa ana amuna kapena
akazi; akadapulumutsa moyo wao wokha ndi cilungamo
cao. 21Pakuti atero Ambuye Yehova, Kopambana kotani nanga
ndikatumizira Yerusalemu maweruzo anga anai owawa, lupanga,
njala, zirombo zoipa, ndi mliri, kuudulira anthu ndi nyama? 22Koma
onani mudzatsala opulumuka m'mwemo amene adzaturutsidwa,
ndiwo ana amuna ndi akazi; taonani, adzaturuka kudza kwa inu;
ndipo mudzaona njira zao, ndi zocita zao; mudzatonthozedwanso
pa zoipa ndazitengera pa Yerusalemu, inde pa zonse
ndazitengerapo. 23Ndipo adzakusangalatsani pamene muona njira
yao, ndi zocita zao; ndipo mudzadziwa kuti sindinazicita kopanda
cifukwa zonse ndinazicita momwemo, ati Ambuye Yehova.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Mtengo wopanda pace

1Ndipo anandidzera mau a Yehova, akuti, 2Wobadwa ndi munthu
iwe, mtengo wampesa uposeranji mtengo uli wonse wina, nthambi
ya mpesa yokhalayo mwa mitengo ya kunkhalango? 3Kodi
atengako mtengo kupanga nao nchito? atengako ciciri kodi
kupacikapo cipangizo ciri conse? 4Taona, auponya kumoto kuuyesa
nkhuni, moto unyeketsa nsonga zace zonse ziwiri, nupserera
pakati pace, kodi ukomera nchito Irf yonse? 5Taonani, pokhala
wamphumphu sunayenera nchito iri yonse, nanga utanyeketsa
moto nupserera udzayeneranso nchito iri yonse? 6Cifukwa cace
atero Ambuye Yehova, Ngati mtengo wampesa pakati pa mitengo
ya kunkhalango ndauponya kumoto ukhale nkhuni, momwemo
ndidzapereka okhala m'Yerusalemu. 7Ndipo ndidzaika nkhope
yanga iwatsutse; adzaturuka kumoto, koma moto udzawatha;
ndipo mudzadziwa kuti Ine ndine Yehova, pakuika Ine nkhope
yanga iwatsutse. 8Ndipo ndidzasandutsa dziko cipululu; popeza
anacita colakwa, ati Ambuye Yehova.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Kusakhulupirika kwa Yerusalemu

1Anandidzeranso mau a Yehova, akuti, 2Wobadwa ndi munthu iwe,
Dziwitsa Yerusalemu zonyansa zace, nuziti, 3Atero Ambuye Yehova
kwa Yerusalemu, Ciyambi cako ndi kubadwa kwako ndiko ku dziko
la Akanani; atate wako anali M-amori, ndi mai wako Mhiti. 4Ndipo
za kubadwa kwako, tsiku lobadwa iwe sanadula ncofu yako,
sanakuyeretsa ndi kukusambitsa ndi madzi, sanakuthira mcere
konse, kapena kukukulunga m'nsaru ai. 5Panalibe diso linakucitira
cifundo, kukucitira cimodzi conse ca izi, kucitira iwe nsoni; koma
unatayidwa kuyere; pakuti ananyansidwa nao moyo wako tsiku la
kubadwa kwake, 6Ndipo popita Ine panali iwepo, ndinakuona
ulikubvimvinizika m'mwazi wako. Pamenepo ndinanena ndi iwe
m'mwazi wako, Khala ndi moyo, inde ndinati kwa iwe m'mwazi
mwako, Khala ndi moyo. 7Ndinakucurukitsa ngati mphundu za
kumunda; ndipo unathululuka ndi kukula kufikira wakongola
nkhope, maere ako anamera, ndi tsitsi lako linamera; koma unali
wamarisece ndi wausiwa. 8Ndipo popita Ine panali iwepo ndi
kukupenya, taona nyengo yako ndiyo nyengo yakukondana;
pamenepo ndinakupfunda copfunda canga, ndi kuphimba
umarisece wako; inde ndinakulumbirira ndi kupangana nawe, ati
Ambuye Yehova, ndipo unakhala wanga. 9Ndipo ndinakusambitsa
ndi madzi, inde ndinakutsuka kukucotsera mwazi wako, ndi
kukudzoza mafuta. 10Ndinakubvekanso ndi nsaru zopikapika, ndi
kukubveka nsapato za cikopa ca katumbu; ndinakuzenenga nsaru
yabafuta, ndi kukuphimba ndi nsaru
yasilika. 11Ndinakukometseranso ndi zokometsera, ndi kuika
zigwinjiri m'manja mwako, ndi unyolo m'khosi
mwako. 12Momwemo ndinaika cipini m'mphuno mwako, ndi
maperere m'makutu mwako, ndi korona wokongola pamutu
pako. 13Ndipo unadzikometsera ndi golidi, ndi siliva, ndi cobvala
cako ndi bafuta ndi silika ndi yopikapika; unadya ufa wosalala, ndi
uci, ndi mafuta; ndipo unali wokongola woposa ndithu, ndipo
unapindula-pindula kufikira unasanduka ufumu. 14Ndi mbiri yako
inabuka mwa amitundu cifukwa ca kukongola kwako; pakuti ndiko
kwangwiro, mwa ulemerero wanga ndinauika pa iwe, ati Ambuye
Yehova.
15Koma unatama kukongola kwako, ndi kucita zacigololo potama
mbiri yako, ndi kutsanulira zigololo zako pa munthu ali yense
wopitapo; unali wace. 16Ndipo unatengako zobvala zako, ndi
kudzimangira misanje ya mawanga mawanga, ndi kucitapo
cigololo; zotere sizinayenera kufika kapena
kucitika. 17Unatenganso zokometsera zako zokoma za golidi wanga
ndi siliva wanga, zimene ndinakupatsa, ndi kudzipangira mafano a

amuna, ndi kucita nao cigololo. 18Unatenganso zobvala zako za nsaru yopikapika, ndi kuwabveka nazo, unaikanso mafuta anga ndi cofukiza canga pamaso pao. 19Ndi mkate wanga ndinakupatsawo, ufa wosalala, ndi mafuta, ndi uci, ndinakudyetsazo, unawaikira izi pamaso pao, zicite pfungo lokoma; kunatero, ati Ambuye Yehova. 20Unatenganso ana ako amuna ndi akazi amene unandibalirawo, ndi kuwapereka nsembe awathe. Zigololo zako zidacepa kodi, 21kuti unawapha ana anga ndi kuwapereka, pakuwapititsa pamoto? 22Ndipo pa zonyansa zako zonse ndi zigololo zako sunakumbukila masiku a ubwana wako, mujaunakhala wamarisece ndi wausiwa, wobvimvinizika m'mwazi wako. 23Ndipo kudacitika utatha zoipa zako zonse, (tsoka iwe, tsoka, ati Ambuye Yehova) 24unadzimangira nyumba yacimphuli, unadzimangiranso ciunda m'makwalala ali onse. 25Unamanga ciunda cako pa mphambano ziri zonse, ndipo unanyansitsa kukongola kwako, ndi kutukula mapazi ako kwa yense wopitako, ndi kucurukitsa cigololo cako. 26Wacitanso cigololo ndi Aaigupto oyandikizana nawe, akulu thupi, ndi kucurukitsa cigololo cako kuutsa mkwiyo wanga. 27Taona tsono, ndakutambasulira dzanja langa, ndi kucepsa gawo lako la cakudya, ndi kukupereka ku cifuniro ca iwo akudana nawe, kwa ana akazi a Afilisti akucita manyazi ndi njira yako yoipa. 28Unacitanso cigololo ndi Aasuri, pakuti unakhala wosakoledwa, inde unacita cigololo nao, koma sunakoledwa. 29Unacurukitsanso cigololo cako m'dziko la Kanani, mpaka dziko la Akasidi, koma sunakoledwa naconso. 30Ha! mtima wako ngwofoka, ati Ambuye Yehova, pakucita iwe izi zonse, ndizo nchito za mkazi wacigololo wouma m'maso. 31Pakumanga nyumba yako yacimphuli pa mphambano ziri zonse, ndi pomanga ciunda cako m'makwalala ali onse, sunakhala ngati mkazi wadama waphindu, popeza unapeputsa mphotho. 32Ndiwe mkazi wokwatibwa wocita cigololo, wolandira alendo m'malo mwa mwamuna wace. 33Anthu amaninkha akazi onse acigololo mphatso, koma iwe umaninkha mabwenzi ako onse mphatso zako ndi kuwalipira, kuti akudzere kucokera ku mbali zonse, kuti acite nawe cigololo. 34M'mwemo usiyana konse ndi akazi ena m'cigololo cako; pakuti palibe wokutsata kucita nawe cigololo; popezanso uwalipira, koma sakupatsa iwe mphotho; potero usiyana nao konse ena.
35Cifukwa cace, wacigololo iwe, tamvera mau a Yehova: 36Atero Ambuye Yehova, Popeza ndalama zako zamwazika, nubvundukuka umarisece wako mwa cigololo cako ndi mabwenzi ako, ndi cifukwa ca mafano onse a zonyansa zako, ndi mwazi wa ana ako umene unawa patsa; 37cifukwa cace taona, ndidzasonkhanitsa mabwenzi ako onse amene wakondwera nao, ndi onse unawakonda, pamodzi

ndi onse unawada; inde ndidzawasonkhanitsira iwe pozungulira ponse, ndi kuwabvundukulira umarisece wako, kuti aone umarisece wako wonse. 38Ndipo ndidzaweruza mlandu wako, monga aweruza akazi acigololo ndi okhetsa mwazi; ndipo ndidzakutengera mwazi wa ukali ndi wa nsanje. 39Ndidzakuperekanso m'dzanja lao, ndipo adzagwetsa nyumba yako yacimphuli, ndi kugumula ziunda zako, nadzakubvula zobvala zako, ndi kulanda zokometsera zako zokongola, nadzakusiya wamarisece ndi wausiwa. 40Ndipo adzamemezera iwe msonkhano, nadzakuponya miyala, ndi kukupyoza ndi malupanga ao. 41Ndipo adzatentha nyumba zako ndi moto, nadzakuweruza pamaso pa akazi ambiri; ndipo ndidzakuleketsa kucita cigololo, ndipo sudzalipiranso mphotho yacigololo. 42M'mwemo ukali wanga udzakhuta nawe, ndi nsanje yanga idzakucokera, ndipo ndidzakhala cete wosakwiyanso. 43Popeza sunakumbukila masiku a ubwana wako, koma wandibvuta nazo zonsezi, cifukwa cace taona, Inenso ndidzakubwezera njira yako pamutu pako, ati Ambuye Yehova; ndipo sudzacita coipa ici coonjezerapo pa zonyansa zako zonse.
44Taona, ali yense wonena miyambi adzakunenera mwambi uwu, wakuti, Monga mace momwemo mwana wace. 45Iwe ndiwe mwana wa mako wonyansidwa naye mwamuna wace ndi ana ace, ndipo iwe ndiwe mng'ono wao wa akulu ako akunyansidwa ndi amuna ao ndi ana ao; mai wako ndiye Mhiti, ndi atate wako ndiye M-amori. 46Ndi mkulu wako ndiye Samariya, wokhala ku dzanja lako lamanzere, iye ndi ana ace akazi; ndi mng'ono wako wokhala ku dzanja lako lamanja ndiye Sodomu ndi ana ace akazi. 47Koma sunayenda m'njira zao, kapena kucita monga mwa zonyansa zao pang'ono pokha; unawaposa iwo m'kubvunda kwako, m'njira zako zonse. 48Pali ine, ati Ambuye Yehova, Sodomu mng'ono wako sanacita, iye kapena ana ace akazi, monga umo unacitira iwe ndi ana ako akazi. 49Taona, mphulupulu ya mng'onowako Sodomu ndi iye, kudzikuza, kucuruka kwa cakudya, ndi kupumula kwa mtambasali, anali nako iye ndi ana ace; ndipo sanalimbitsa dzanja la wosauka ndi wosowa. 50Ndipo anadzikuza, nacita conyansa pamaso panga; cifukwa cace ndinawacotsa pakuciona. 51Ngakhale Samariya sanacita theka la zocimwa zako, koma unacurukitsa zonyansa zako kuwaposa iwowa, ndi kuika abale ako olungama ndi zonyansa zako zonse unazicita. 52Usenzenso manyazi ako, iwe wakuweruza abale ako mwa zocimwa zako unazicita monyansa koposa iwowa; iwo akuposa iwe m'cilungamo cao, nawenso ucite manyazi nusenze manyazi ako, popeza waika abale ako olungama. 53Ndipo ndidzabweza undende wao, undende wa Sodomu ndi ana ace, ndi undende wa Samariya ndi ana ace, ndi

undede wa andende ako pakati pao; 54kuti usenze manyazi ako,
ndi kuti ucite manyazi cifukwa ca zonse unazicita
pakuwatonthoza. 55Ndipo abale ako Sodomu ndi ana ace
adzabwerera umo unakhalira kale; ndi iwe ndi ana ako
mudzabwerera umo munakhalira kale. 56Ndipo sunakamba za
mbale wako Sodomu pakamwa pako tsiku la kudzikuza
kwako; 57cisanabvundukuke coipa cako monga nthawi ya citonzo
ca ana akazi a Aramu, ndi onse akumzungulira iye, ana akazi a
Afilisti akupeputsa pozungulira ponse. 58Wasenza coipa cako ndi
zonyansa zako, ati Yehova. 59Pakuti atero Ambuye Yehova,
Ndidzacita ndi iwe monga umo unacitira; popeza wapepula lumbiro
ndi kutyola pangano. 60Koma ndidzakumbukila Ine pangano langa
ndi iwe m'masiku a ubwana wako, ndipo ndidzakhazikitsa pangano
losatha nawe. 61Pamenepo udzakumbukila njira zako ndi kucita
manyazi, pakulandira abale ako akuru ndi ang'ono; ndipo
ndidzakupatsa awa akhale ana ako akazi, angakhale sali a
pangano lako. 62Pakuti ndidzakhazikitsa pangano langa ndi iwe,
ndipo udzadziwa kuti Ine ndine Yehova; 63kuti uzikumbukila ndi
kucita manyazi ndi kusatsegulanso pakamwa pako konse, cifukwa
ca manyazi ako, pamene ndikufafanima zonse unazicita, ati
Ambuye Yehova.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Fanizo la ziombankhanga ziwiri ndi mpesa

1Ndipo anandidzera mau a Yehova, akuti, 2Wobadwa ndi munthu
iwe, ipha mwambi, nunene fanizo kwa nyumba ya Israyeli, 3nuziti,
Atero Ambuye Yehova, Ciombankhanga cacikuru ndi mapiko akuru,
ndi maphiphi atali, odzala nthenga ca mathotho-mathotho, cinafika
ku Lebano, nicitenga nsonga ya mkungudza, 4cinabudula nsonga
yosomphoka ya nthambi zace zanthete, ndi kumuka nayo ku dziko
la malonda, cinaiika m'mudzi wa amalonda. 5Cinatengakonso
mbeu ya m'dziko, ndi kuibzala m'nthaka yokoma, cinaiika panali
madzi ambiri, cinaioka ngati mtengo wamsondodzi. 6Ndipo
inaphuka, nikhala mpesa wotambalala wofupi msinkhu, nthambi
zace zinapindikira momwe, ndi mizu yace pansi pace, nikhala
mpesa, nuonetsa nthambi ndi kuphuka mphukira. 7Panalinso
ciombankhanga cina cacikuru, ndi mapiko akuru, ndi nthenga
zambiri; ndipo taona, mpesa uwu unacipindira mizu yace,
nucilunjikitsira nthambi zace, kucokera pookedwa pace, kuti
ciuthirire madzi. 8Unaokedwa mu nthaka yabwino kuli madzi
ambiri, kuti uphuke nthambi, nubale zipatso, nukhale mpesa
wabwino. 9Uziti, Atero Ambuye Yehova, Udzakondwa kodi?
sadzausula ndi kudula zipatso zace, kuti uume, kuti masamba ace
onse ophuka aume, ngakhale palibe mphamvu yaikuru, kapena
anthu ambiri akuuzula? 10Inde ungakhale waokedwa udzakondwa
kodi? sudzauma ciumire kodi pakuuomba mphepo ya kum'mawa?
udzauma pookedwa apo udaphuka.
11Ndipo anandidzera mau a Yehova, akuti. 12Uziti tsono kwa
nyumba ya mpandukoyi, Simudziwa kodi izi nciani? Uziti, Taonani
mfumu ya ku Babulo inadza ku Yerusalemu, nitenga mfumu yace
ndi akalonga ace, nibwera nao kuti iye ku Babulo; 13nitenga wa
mbumba yacifumu, nicita naye pangano, nimlumbiritsa, nicotsa
amphamvu a m'dziko; 14kuti ufumuwo ukhale wopepuka, kuti
usadzikweze, koma kuti pakusunga pangano lace ukhale. 15Koma
anapandukira ndi kutuma mithenga yace ku Aigupto, kuti ampatse
akavalo ndi anthu ambiri. Adzapindula kodi? adzapulumuka
wakucita izi? atyole pangano ndi kupulumuka kodi? 16Pali Ine, ati
Ambuye Yehova, pamalo pokhala mfumu, imene idamcititsa
ufumu, imene anapeputsa lumbiro lace, imene anatyola pangano
lace, adzafa pamodzi ndi iye pakati pa Babulo. 17Ndipo Farao ndi
nkhondo yace yaikuru, ndi khamu lace launyinji, sadzacita pamodzi
naye kunkhondo, pakuunda mtumbira, ndi kumanga malinga,
kulikha anthu ambiri. 18Pakuti anapepula lumbiro, ndi kutyola
pangano, angakhale anapereka dzanja lace; popeza anacita izi
zonse sadzapulumuka. 19Cifukwa cace atero Ambuye Yehova, Pali
Ine, lumbiro langa, analipepula, ndi pangano langa analityola,

ndidzawabweza pamutu pace. 20Ndidzamphimbanso ndi ukonde
wanga, nadzakodwa iye mu msampha wanga; ndipo ndidzadza
naye ku Babulo, ndi kunena naye komweko mlandu wa kulakwa
kwace anandilakwira nako. 21Ndipo othawa ace onse m'magulu
ace onse adzagwa ndi lupanga, ndi otsala adzabalalitsidwa ku
mphepo zonse; ndipo mudzadziwa kuti Ine Yehova ndanena.
22Atero Ambuye Yehova, Ndidzatenganso nsonga ya mkungudza
wautali ndi kulika; ndidzabudula nsonga yosomphoka'ya nthambi
zace zanthete, ndi kuioka pa phiri lalitali lothubvuka; 23pa phiri
lothubvuka la Israyeli ndidzaioka, ndipo idzaphuka nthambi ndi
kubala zipatso, nidzakhala mkungudza wokoma, ndi m'munsi
mwace mudzakhala mbalame ziri zonse za mapiko ali onse; mu
mthunzi wa nthambi zace zidzabindikira. 24Ndipo mitengo yonse
ya kuthengo idzadziwa kuti Ine Yehova ndatsitsa mtengo
wosomphoka, ndakuza mtengo waung'ono, ndaumitsa mtengo
wauwisi, ndi kuphukitsa mtengo wouma; Ine Yehova ndanena ndi
kucicita.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Udindo ndi wace wace wa munthu

1Ndipo anandidzera mau a Yehoya, akuti, 2Mutani inu ndi kunena
mwambi uwu za dziko la Israyeli, wakuti, Atate adadya mphesa
zosacha, ndi mano a ana ayayamira. 3Pali Ine, ati Ambuye Yehova,
simudzaonanso cifukwa ca kunena mwambiwu
m'Israyeli. 4Taonani, miyoyo yonse ndi yanga, monga moyo wa
atate momwemonso moyo wa mwana, ndiyo yanga; moyo
wocimwawo ndiwo udzafa. 5Koma munthu akakhala wolungama,
nakacita ciweruzo ndi cilungamo, 6wosadya pamapiripo,
wosakweza maso ace ku mafano a nyumba ya Israyeli, wosaipsa
mkazi wa mnansi wace, kapena kuyandikira mkazi
ataoloka, 7wosasautsa munthu ali yense, koma wambwezera
wangongole cigwiriro cace, wosatenga zofunkha, anampatsa
wanjala cakudya cace, nabveka wamarisece ndi
cobvala, 8wosapereka molira phindu, wosatenga coonjezerapo
wobweza dzanja lace lisacite cosalungama, woweruza zoona pakati
pa munthu ndi mnzace, 9amayenda m'malemba anga, nasunga
maweruzo anga kucita cokhulupirika; iye ndiye wolungama,
adzakhala ndi moyo ndithu, anena Ambuye Yehova. 10Akabala
mwana ndiye mkhungu, wokhetsa mwazi, wocita cimodzi ca
izi, 11wosacita zabwino zonse zija, koma anadyanso pamapiri,
naipsa mkazi wa mnansi wace, 12nasautsa osauka ndi osowa,
natenga zofunkha, wosabwezera cigwiriro, nakweza maso ace
kumafano, nacita conyansa, 13napereka molira phindu, nalandira
coonjezerapo; adzakhala ndi moyo uyu kodi? sadzakhala ndi moyo,
anacita zonyansa izi zonse; kufa adzafadi, niwazi wace
umkhalira. 14Taona tsono, yemweyo akabala mwana uyu, naona
zocimwa zonse adazicita atate wace, naopa wosacita
zoterezo, 15wosadya pamapiri, kapena kukweza maso ace ku
mafano a nyumba ya Israyeli, wosaipsa mkazi wa mnansi
wace, 16kapena kusautsa wina ali yense, wosatenga cigwiriro,
wosatenga zofunkha; koma anapatsa wanjala cakudya cace,
nabveka wamarisece ndi cobvala, 17naletsa dzanja lace pa
wozunzika, wosalandira phindu kapena coonjezerapo, wocita
maweruzo anga, nayenda m'malemba anga; uyu sadzafera
mphulupulu ya atate wace, adzakhala ndi moyo ndithu. 18Atate
wace, popeza anazunza cizunzire, nafunkha za mbale wace, nacita
cimene siciri cabwino pakati pa anthu ace, taona, adzafa mu
mphulupulu yace. 19Koma inu mukuti, Alekeranji mwana kusenza
mphulupulu za atate wace? Mwanayo akacita ciweruzo ndi
cilungamo, nakasunga malemba anga onse, ndi kuwacita,
adzakhala ndi moyo ndithu. 20Moyo wocimwawo ndiwo udzafa;
mwana sadzasenza mphulupulu zaatate wace, ndi atate

sadzasenza mphulupulu za mwana; cilungamo ca wolungama cidzamkhalira, ndi coipa ca woipa cidzamkhalira, 21Koma woipayo akabwerera kusiya macimo ace onse adawacita nakasunga malemba anga onse, ndi kucita ciweruzo ndi cilungamo, adzakhala ndi moyo ndithu, sadzafa. 22Nnena cimodzi conse ca zolakwa zace zonse adazicita cidzakumbukika cimtsutse; m'cilungamo cace adacicita adakhala ndi moyo. 23Ngati ndikondwera nayo imfa ya woipa? ati Ambuye Yehova, si ndiko kuti abwerere kuleka njira yace, ndi kukhala ndi moyo? 24Koma wolungamayo akabwerera kuleka cilungamo cace, nakacita mphulupulu, ndi kucita monga mwa zonyansa zonse azicita woipa, adzakhala ndi moyo kodi? Nnena cimodzi ca zolungama zace zonse adzazicita cidzakumbukika m'kulakwa kwace analakwa nako, ndi m'kucimwa kwace anacimwa nako; momwemo adzafa. 25Koma mukuti, Njira ya Ambuye njosayenera. Tamvera tsono nyumba ya Israyeli, Kodi njira yanga njosayenera? njira zanu si ndizo zosayenera? 26Wolungamayo akatembenukira kuleka cilungamo cace, nakacita mphulupulu, adzafa momwemo; m'mphulupulu yace adaicita adzafa. 27Ndipo woipayo akatembenukira kuleka coipa cace adacicita, nakacita ciweruzo ndi cilungamo, adzapulumutsa moyo wace. 28Popeza anasamalira, natembenukira kuleka zolakwa zace zonse adazicita, adzakhala ndi moyo ndithu, sadzafa. 29Koma nyumba ya Israyeli imanena, Njira ya Ambuye njosayenera, Inu, nyumba ya Israyeli, kodi njira zanga nzosayenera? njira zanu si ndizo zosayenera? 30Cifukwa cace ndidzakuweruzani inu, nyumba ya Israyeli, yense monga mwa njira zace, ati Ambuye Yehova. Bwererani, nimutembenukire kuleka zolakwa zanu zonse, ndipo simudzakhumudwa nazo, ndi kuonongeka nayo mphulupulu. 31Tayani, ndi kudzicotsera zolakwa zanu zonse zimene munalakwa nazo, ndi kudzifunira mtima watsopano, ndi mzimu watsopano; pakuti mudzaferanji inu, nyumba ya Israyeli? 32Pakuti sindikondwera nayo imfa ya wakufayo, ati Ambuye Yehova; cifukwa cace bwererani, nimukhale ndi moyo.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Fanizo la mkango waukazi, ndi la mpesa

1Ndipo iwe, takwezera akalonga a Israyeli nyimbo ya maliro, 2uziti,
Mai wako ndi ciani? Mkango waukazi unabwanthama mwa
mikango, unalera ana ace pakati pa misona. 3Ndipo unalera
mmodzi wa ana ace, iye nasanduka msona, unaphunzira kugwira
nyama, unalusira anthu. 4Mitundu ya anthu idamva mbiri yace,
unagwidwa m'mbuna mwao; ndipo anadza nao ndi zokowera ku
dziko la Aigupto. 5Pakuona tsono waukaziwo, kuti unalindirira, ndi
kuti ciyembekezo cace cidatha, unatenga wina wa ana ace,
numsandutsa msona. 6Ndipo unayendayenda pakati pa mikango,
nukhala msona, nuphunzira kugwira nyama, nulusira anthu. 7Ndipo
unadziwa amasiye ao, nupasula midzi yao, ndipo dziko ndi kudzala
kwace linasanduka labwinja, cifukwa ca phokoso la kubangula
kwace. 8Pamenepo mitundu ya anthu inadzipereka kuukola
kucokera ku maiko a ku mbali zonse, niuphimba ndi ukonde wao,
nugwidwa uwu m'mbuna mwao. 9Nauika m'citatanga ndi
zokowera, nadza nao kwa mfumu ya ku Babulo; anaulonga
m'malinga, kuti mau ace asamvekenso pa mapiri a Israyeli.
10Mai wako ananga mpesa wookedwa kumadzi; muja anakhala
mumtendere unabala zipatso, wodzala ndi nthambi, cifukwa ca
madzi ambiri. 11Ndipo unali nazo ndodo zolimba zikhale ndodo
zacifumu, za ocita ufumu, ndi msinkhu wao unakula kufikira
kumitambo, nizinaoneka m'kusomphoka kwao pakati pa nthambi
zace zambiri. 12Koma unazulidwa mwaukali, unaponyedwa pansi
ndi mphepo ya kum'mawa, inaumitsa zipatso zace, ndodo zace
zolimba zinatyoka ndi kuuma, moto unazitha. 13Ndipo tsopano
waokedwa m'cipululu m'dziko louma ndi la ludzu. 14Unaturukanso
moto ku ndodo za ku nthambi zace, unatha zipatso zace;
m'mwemo ulibe ndodo yolimba ikhale ndodo yacifumu ya kucita
ufumu. Iyi ndi nyimbo idzakhala nyimbo ya maliro.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Macimo a Aisrayeli citurukire iwo m'dziko la Aigupto

1Ndipo kunali caka cacisanu ndi ciwiri, mwezi wacisanu; tsiku
lakhumi la mwezi, anadza akulu ena a Israyeli kufunsira kwa
Yehova, nakhala pansi iwowa pamaso panga. 2Ndipo anandidzera
mau a Yehova, akuti, 3Wobadwa ndi munthu iwe, lankhula ndi
akulu a Israyeli, nunene nao, Atero Ambuye Yehova, Mwadza kodi
kufunsira kwa Ine? Pali Ine, sindidzafunsidwa ndi inu, ati Ambuye
Yehova. 4Udzawaweruza kodi, wobadwa ndi munthu iwe?
udzawaweruza? uwadziwitse zonyansa za makolo ao, 5nunene nao,
Atero Ambuye Yehova, Tsiku lija ndinamsankha Israyeli, ndi
kukwezera mbeu ya nyumba ya Yakobo dzanja langa, ndi
kudzidziwitsa kwa iwo m'dziko la Aigupto, pakuwakwezera dzanja
langa, ndi kuti, Ine ndine Yehova Mulungu wanu; 6tsiku lomwelo
ndinawakwezera dzanja langa kuwaturutsa m'dziko la Aigupto,
kumka nao ku dziko ndinawazondera, moyenda mkaka ndi uci,
ndilo lokometsetsa mwa maiko onse; 7ndipo ndinanena nao, Ali
yense ataye zonyansa za pamaso pace, nimusadzidetsa ndi
mafano a Aigupto; Ine ndine Yehova Mulungu wanu. 8Koma
anapandukira Ine, osafuna kundimvera Ine, sanataya yense
zonyansa pamaso pace, sanaleka mafano a Aigupto; pamenepo
ndidati ndiwatsanulire ukali wanga, kuwakwaniritsira mkwiyo
wanga m'dziko la Aigupto. 9Koma ndinacicita cifukwa ca dzina
langa, kuti lisadetsedwe pamaso pa amitundu amene anakhala
pakati pao, amene pamaso pao ndinadzidziwitsa kwa iwo,
pakuwaturutsa m'dziko la Aigupto. 10Momwemo ndinaturuka nao
m'dziko la Aigupto, ndi kulowa nao kucipululu. 11Ndinawapatsanso
malemba anga, ndi kuwadziwitsa maweruzo anga, ndiwo munthu
akawacita adzakhala nao ndi moyo. 12Ndipo ndinawapatsanso
masabata anga akhale cizindikilo pakati pa Ine ndi iwo, kuti adziwe
kuti Ine ndine Yehova wakuwapatula. 13Koma nyumba ya Israyeli
inapaodukira Ine m'cipululu, sanayenda m'malemba anga,
nanyoza maweruzo anga, amene, munthu akawacita adzakhala
nao ndi moyo; ndi masabata anga anawaipsa kwambiri; pamenepo
ndidati ndiwatsanulire ukali wanga m'cipululu kuwatha. 14Koma
ndinacicita cifukwa ca dzina langa, kuti lisaipsidwe pamaso pa
amitundu amene ndinawaturutsa pamaso pao. 15Ndipo
ndinawakwezeranso dzanja langa m'cipululu, kusawalowetsa
m'dzikolo ndidawapatsa, moyenda mkaka ndi uci, ndilo
lokometsetsa mwa maiko onse; 16popeza ananyoza maweruzo
anga, osayenda m'malemba anga, naipsa masabata anga; pakuti
mitima yao inatsata mafano ao. 17Koma diso langa lidawaleka
osawaononga, sindinawatha onse m'cipululu. 18Ndipo ndinati kwa
ana ao m'cipululu, Musamayenda m'malemba a atate anu,

musawasunga maweruzo ao, kapena kudzidetsa ndi mafano
ao; 19Ine ndine Yehova Mulungu wanu, muziyenda m'malemba
anga, ndi kusunga maweruzo anga, ndi kuwacita; 20muzipatulanso
masabata anga, ndipo adzakhala cizindikilo pakati pa Ine ndi inu,
kuti mudziwe kuti Ine ndine Yehova Mulungu wanu. 21Koma anawo
anapandukira Ine, sanayenda m'malemba anga, kapena kusunga
maweruzo anga kuwacita, amene munthu akawacita adzakhala
nao ndi moyo; anaipsa masabata anga; pamenepo ndinati
ndidzawatsanulira ukali wanga, kuwakwaniritsira mkwiyo wanga
m'cipululu. 22Koma ndinabweza dzanja langa ndi kucicita, cifukwa
ca dzina langa; kuti lisaipsidwe pamaso pa amitundu, amene
ndinawaturutsa pamaso pao. Ndinawakwezeranso dzanja langa
m'cipululu, 23kuti ndidzawabalalitsa mwa amitundu, ndi
kuwamwaza m'maiko; 24popeza sanacita maweruzo anga, koma
ananyoza malemba anga, naipsa masabata anga, ndi maso ao
anatsata mafano a atate ao. 25Momwemonso ndinawapatsa
malemba amene sanali abwino, ndi maweruzo osakhala nao ndi
moyo; 26ndinawadetsanso m'zopereka zao; pakuti anapititsa
pamoto onse oyamba kubadwa kuti ndiwapasule; kuti adziwe kuti
Ine ndine Yehova.
27Cifukwa cace wobadwa ndi munthu iwe, lankhula ndi nyumba ya
Israyeli, nunene nao, Atero Ambuye Yehova, Mwa icinso atate anu
anandicitira mwano pakundilakwira Ine. 28Nditafika nao m'dzikolo
ndinawakwezera dzanja langa kuwapatsa ilo, anapenya citunda ciri
conse cacitali, ndi mtengo uli wonse wagudugudu, naphera
pomwepo nsembe zao, napetekapo nsembe zao zondiputa, aponso
anacita pfungo lao lokoma, nathiraponso nsembe zao
zothira. 29Pamenepo ndinanena nao, Msanje wotani uwu
mumapitako? Momwemo dzina lace lichedwa Msanje, mpaka lero
lino. 30Cifukwa cace uziti kwa nyumba ya Israyeli, Atero Ambuye
Yehova, Mudzidetsa kodi monga umo anacitira makolo anu? mucita
cigololo kodi kutsata zonyansa zao? 31ndipo popereka zopereka
zanu popititsa ana anu pamoto, mudzidetsa kodi ndi mafano anu
onse mpaka lero lino? ndipo kodi ndidzafunsidwa ndi inu, nyumba
ya Israyeli? Pali Ine, ati Ambuye Yehova, sindidzafunsidwa ndi
inu; 32ndi ici cimauka mumtima mwanu sicidzacitika, umo mukuti,
Tidzakhala ngati amitundu, ngati mabanja a m'maiko, kutumikira
mtengo ndi mwala.

Mulungu adzabweza Israyeli kucokera kobalalikidwa iwo

33Pali Ine, ati Ambuye Yehova, zedi ndi dzanja lamphamvu, ndi
mkono wotambasuka, ndi ukali wotsanulidwa, ndidzakhala mfumu
yanu. 34Ndipo ndidzakuturutsani mwa mitundu ya anthu, ndi
kukusonkhanitsani m'maiko munabalalikamo ndi dzanja
lamphamvu, ndi mkono wotambasuka, ndi ukali

wotsanulidwa. 35Ndipo ndidzalowa nanu m'cipululu ca mitundu ya
anthu, ndi kukuweruzani komweko popenyana maso. 36Monga
ndinaweruza makolo anu m'cipululu ca dziko la Aigupto,
momwemo ndidzaweruza inu, ati Ambuye Yehova. 37Ndipo
ndidzakupititsani pansi pa ndodo ya mbusa ndi kukulowetsani
m'cimango ca cipangano; 38ndipo ndidzasankhula mwa inu
opanduka ndi ondilakwira, ndidzawaturutsa m'dziko logoneramo
iwo; koma sadzalowa m'dziko la Israyeli; motero mudzadziwa kuti
Ine ndine Yehova. 39Ndipo inu, nyumba ya Israyeli, atero Ambuye
Yehova, mukani, tumikirani yense mafano ace, ndi m'tsogolo
momwe, popeza simundimvera Ine; koma musaipsanso dzina
langa lopatulika ndi zopereka zanu ndi mafano anu. 40Pakuti pa
phiri langa lopatulika, pa phiri lothubvuka la Israyeli, ati Ambuye
Yehova, pomwepo onse a nyumba ya Israyeli, onsewo
adzanditumikira Ine m'dzikomo; pomwepo ndidzawalandira, ndi
pomwepo ndidzafuna nsembe zanu zokweza, ndi zoyamba za
msonkho wanu, pamodzi ndi zopatulika zanu zonse. 41Ngati pfungo
lokoma ndidzakulandirani pakukuturutsani mwa mitundu ya anthu,
ndipo ndidzakusonkhanitsani kukucotsani m'maiko
munabalalikiramo, ndipo ndidzazindikirika Woyera mwa inu
pamaso pa amitundu. 42Ndipo mudzadziwa kuti Ine ndine Yehova,
pakukulowetsani Ine m'dzil ko la Israyeli, m'dzikoli ndinalikwezera
dzanja langa kulipereka kwa makolo anu. 43Ndi pomwepo
mudzakumbukila njira zanu, ndi zonse mudazicita ndi kudzidetsa
nazo, ndipo mudzakhala onyansa pamaso pa inu nokha, cifukwa ca
zoipa zanu zonse mudazicita. 44M'mwemo mudzadziwa kuti Ine
ndine Yehova nditacita nanu cifukwa ca dzina langa, si monga mwa
njira zanu zoipa, kapena monga mwa macitidwe anu obvunda,
nyumba ya Israyeli inu, ati Ambuye Yehova.
45Ndipo anandidzera mau a Yehova, akuti, 46Wobadwa ndi munthu
iwe, lozetsa nkhope yako njira ya kumwera, nubenthulire mau
kumwera, nunenere nkhalango ya kuthengo la kumwera kwa
Yuda; 47nuziti kwa nkhalango ya kumwera kwa Yuda, Tamvera mau
a Yehova, Atero Ambuye Yehova, Taona ndidzayatsa moto mwa
iwe, udzanyeketsa mtengo uli wonse wauwisi mwa iwe, ndi mtengo
uli wonse wouma; malawi amoto sadzazimika, ndi nkhope zonse
kuyambira kumwera kufikira kumpoto zidzapsa nao. 48Ndi anthu
onse adzaona kuti Ine Yehova ndinauyatsa,
sudzazimika. 49Pamenepo ndinati, Ha, Ambuye Yehova!
anandinena, Wonena mafanizo uyu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Lupanga la Yehova

1Ndipo anandidzera mau a Yehova, akuti, 2Wobadwa ndi munthu
iwe, lozetsa nkhope yako ku Yerusalemu, nuwabenthulire mau
malo opatulikawa, nunenere dziko la Israyeli kulitsutsa; 3nuziti kwa
dziko la Israyeli, Atero Yehova, Taona Ine ndine wotsutsana nawe,
ndidzasolola lupanga langa m'cimace, ndi kukulikhira olungama
ndi oipa. 4Popeza ndidzakulikhira olungama ndi oipa, cifukwa cace
lupanga langa lidzasololokera anthu onse, kuyambira kumwera
kufikira kumpoto; 5ndi anthu onse adzadziwa kuti Ine Yehova
ndasolola lupangalanga m'cimace, silidzabwereranso. 6Koma
wobadwa ndi munthu iwe, usa moyo, ndi kuduka msana, ndi
kuwawa mtima, uuse moyo pamaso pao. 7Ndipo kudzakhala
akanena ndi iwe, Uusa moyo cifukwa ninji? uzikati, Cifukwa ca
mbiri; pakuti ikudza, ndi mtima uli wonse udzasungunuka, ndi
manja onse adzalenda, ndi mzimu uli wonse udzakomoka, ndi
maondo onse adzaweyeseka ngati madzi; taona irinkudza, inde
idzacitika, ati Ambuye Yehova.
8Ndipo anandidzera mau a Yehova, akuti, 9Wobadwa ndi munthu
iwe, nenera ndi kuti, Atero Yehova, Nena, Lupanga, lupanga
lanoledwa, latuulidwanso; 10lanoledwa kuti liphetu, lituulidwa kuti
linge mphezi; tisekererepo kodi? ndilo ndodo yacifumu ya mwana
wanga, yopeputsa mtengo uli wonse. 11Ndipo analipereka alituule,
kuti acite nalo lupangali analinola, inde analituula kulipereka
m'dzanja la wakupha. 12Pfuula ndi kulira, wobadwa ndi munthu
iwe, pakuti likhalira pa anthu anga, likhalira pa akalonga onse a
Israyeli, laperekedwa kulupanga pamodzi ndi anthu anga; cifukwa
cace panda pancafu pako. 13Pakuti pali kuyesedwa; ndipo nanga
ndodo yacifumu yopeputsa ikapanda kukhalanso? ati Ambuye
Yehova. 14Ndipo wobadwa ndi munthu iwe, nenera, nuombe manja,
lupanga lipitirize katatu, lupanga la wolasidwa ndilo lupanga la
wolasidwa wamkuruyo, limene liwazinga. 15Ndalozetsa nsonga ya
lupanga ku zipata zao zonse, kuti mtima wao usungunuke, ndi
kukhumudwa kwao kucuruke; ha! analituula linyezimire,
analisongoza liphe, 16Udzisonkhanitsire pamodzi, muka ku dzanja
lamanja; undandalitsa nkhondo kumuka kulamanzere; kuli konse
ilozako nkhope yako. 17Inenso ndidzaomba manja anga, ndipo
ndidzakukwaniritsa ukali wanga; Ine Yehova ndanena.
18Ndipo mau a Yehova anandidzera, akuti, 19Wobadwa ndi munthu
iwe, udziikire njira ziwiri zodzera lupanga la mfumu ya ku Babulo;
zonse ziwiri zicokere dziko lomwelo; nulembe cizindikilo colozera,
ucilembe pa mphambano ya njira ya kumudzi. 20Uiike njira yodzera
lupanga kumka ku Raba wa ana a Amoni, ndi ya ku Yuda ku
Yerusalemu, mudzi walinga. 21Pakuti mfumu ya ku Babulo aima pa

mphambano ya njira, polekana njira ziwirizo, kuti aombeze maula;
agwedeza mibvi, afunsira kwa aterafi, apenda ndi
ciwindi. 22M'dzanja lace lamanja muli ula wa ku Yerusalemu, kuika
zogundira, kutsegula pakamwa pa kupha, kukweza mau ndi
kupfuula, kuikira zitseko zogundira, kuundira mtumbira, kumanga
malinga. 23Ndipo kudzakhala ngati kuombeza konyenga pamaso
pa iwo amene anawalumbirira malumbiro; koma akumbutsa
mphulupulu kuti akodwe.
24Cifukwa cace atero Ambuye Yehova, Popeza mwakumbutsa
mphulupulu yanu pobvumbuluka zolakwa zanu, kotero kuti macimo
anu aoneka m'zonse muzicita, popeza mukumbukika,
mudzagwidwa ndi dzanja. 25Ndipo iwe wolasidwa woipa, kalonga
wa Israyeli, amene lafika tsiku lako, nthawi ya mphulupulu
yotsiriza; 26atero Ambuye Yehova, Cotsa cilemba, bvula korona,
ufumu sudzakhalanso momwemo, kweza copepuka, cepsa
cokwezeka. 27Ndidzagubuduza gubuduza gubuduza ufumu uno,
sudzakhalanso kufikira akadza Iye mwini ciweruzo; ndipo
ndidzaupereka kwa Iye.
28Ndipo iwe wobadwa ndi munthu, nenera, nuziti, Atero Ambuye
Yehova za ana a Amoni, ndi za citonzo cao; nuziti, Lupanga,
lupanga lasololedwa, latuulidwa, kuti likaphe, kuti liononge, likhale
lonyezimira. 29Akuonera zopanda pace, akuombezera mabodza,
lupanga likugoneka pa makosi a oipa olasidwa, amene lafika tsiku
lao nthawi ya mphulupulu yotsiriza. 30Ulibwezere m'cimace.
Pamalo unalengedwapo m'dziko la kubadwa kwako
ndidzakuweruza. 31Ndipo ndidzakutsanulira mkwiyo wanga,
ndidzakuuzira ndi moto wa kuzaza kwanga, ndidzakuperekanso
m'manja mwa anthu ankharwe odziwa kuononga. 32Udzakhala
ngati nkhuni ya pamoto, mwazi wako udzakhala pakati pa dziko,
sudzakumbukikanso; pakuti Ine ndine Yehova ndacinena.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Macimo oopsa a Yerusalemu

1Anandidzeransomau a Yehova, akuti, 2Ndipo iwe wobadwa ndi
munthu, udzaweruza, udzauweruza mudziwo wa mwazi kodi?
uudziwitse tsono zonyansa zace zonse. 3Nuziti, Atero Ambuye
Yehova, Ndiwo mudzi wokhetsa mwazi pakati pace, kuti nthawi
yace ifike, nudzipangire mafano kudzidetsa nao. 4Waparamula nao
mwazi wako, waukhetsa, nudetsedwa nao mafano ako
udawapanga, nuyandikizitsa masiku ako, wafikiranso zako zako;
cifukwa cace ndakuika ukhale citonzo ca amitundu ndi coseketsa
ca maiko onse. 5Okhala pafupi ndi okhala patali adzakuseka
pwepwete, wodetsedwa dzina iwe, wodzala ndi kusokosera. 6Taona
akalonga a Israyeli, yense monga mwa mphamvu yace, akhala
mwa iwe, kuti akhetse mwazi. 7Mwa iwe anapepula atate ndi mai,
pakati pa iwe anamcitira mlendo momzunza, mwa iwe anazunza
ana amasiye, ndi mkazi wamasiye. 8Wanyoza zopatulika zanga,
waipsa masabata anga. 9Anthu oneneza anali mwa iwe, kuti
akhetse mwazi; ndipo anadya pamapiri mwa iwe, pakati pa iwe
anacita zamanyazi. 10Anabvula umarisece wa atate ao mwa iwe,
mwa iwe anacepsa wodetsedwa ndi kooloka kwace. 11Ndipo wina
anacita conyansa ndi mkazi wa mnansi wace, winanso wadetsa
mpongozi wace mwamanyazi, ndi wina mwa iwe anaipitsa mlongo
wace mwana wamkazi wa atate wace. 12Analandira mphotho mwa
iwe kukhetsa mwazi, walandira phindu loonjezerapo,
wanyengerera anansi ako ndi kuwazunza, ndipo wandiiwala Ine, ati
Ambuye Yehova. 13Taona, ndaomba manja pa phindu lako
lonyenga waliona, ndi pa mwazi wokhala pakati pako. 14Mtima
wako udzaimika kodi, manja ako adzalimbikira masikuwo
ndidzacita nawe? Ine Yehova ndanena, ndidzacicita. 15Ndipo
ndidzakumwaza mwa amitundu, ndi kukubalalitsa m'maiko, ndi
kukuthera zodetsa zako zikucokere. 16Ndipo udzaipsidwa mwa iwe
wekha pamaso pa amitundu; motero udzadziwa kuti Ine ndine
Yehova.
17Ndipo mau a Yehova anandidzera, akuti, 18Wobadwa ndi munthu
iwe, nyumba ya Israyeli yandikhalira mphala; onsewo ndiwo
mkuwa, ndi seta, ndi citsulo, ndi ntobvu, m'kati mwa ng'anjo;
ndiwo mphala zasiliva. 19Cifukwa cace atero Ambuye Yehova,
Popeza mwasanduka mphala nonsenu, cifukwa cace taonani,
ndidzakusonkhanitsani m'kati mwa Yerusalemu. 20Monga
asonkhanitsamtapo wa siliva, ndi mkuwa, ndi citsulo, ndi ntobvu,
ndi seta, m'kati mwa ng'anjo, kuzibvukutira moto, kuzisungunula
momwemo, ndidzakusonkhanitsani mu mkwiyo wanga ndi ukali
wanga, ndi kukuikani komweko, ndi kukusungunulani. 21Inde
ndidzakusonkhanitsani, ndi kukubvukutirani ndi moto wa kuzaza

kwanga, ndipo mudzasungunuka pakati pace. 22Monga siliva
asungunuka m'kati mwa ng'anjo, momwemo inu mudzasungunuka
m'kati mwace; motero mudzadziwa kuti Ine Yehova
ndakutsanulirani ukali wanga.
23Nandidzeranso mau a Yehova, akuti, 24Wobadwa ndi munthu iwe,
nena ndi Yuda, Iwe ndiwe dziko losayeretsedwa, losabvumbwa
mvula tsiku la ukalilo. 25Pali ciwembu ca aneneri ace pakati pace,
ngati mkango wobangula womwetula nyama, analusira miyoyo,
alanda cuma ndi za mtengo wace, acurukitsa amasiye pakati
pace. 26Ansembe ace acitira coipa cilamulo canga, nadetsa
zopatulika zanga, sasiyanitsa pakati pa zopatulika ndi
zosapatulika, ndipo sazindikiritsa anthu pakati pa zodetsa ndi
zoyera, nabisira masabata anga maso ao; ndipo Ine ndidetsedwa
pakati pao. 27Akalonga ace m'kati mwace akunga afisi akumwetula
nyama, kukhetsa mwazi, kuononga miyoyo, kuti aone phindu
lonyenga. 28Ndipo aneneri ao anawamatira ndi dothi losapondeka,
ndi kuonera zopanda pace, ndi kuwaombezera mabodza, ndi kuti,
Atero Ambuye Yehova posanena Yehova. 29Anthu a m'dziko
anazunzazunza, nalandalanda mwaciwawa, napsinja ozunzika ndi
aumphawi, nazunza mlendo wopanda cifukwa. 30Ndipo
ndinafunafuna munthu pakati pao wakumanganso linga, ndi
kuimira dziko popasukira pamaso panga, kuti ndisaliononge; koma
ndinapeza palibe. 31Cifukwa cace ndinawatsanulira ukali wanga,
ndawatha ndi moto wa kuzaza kwanga, njira yao yao ndinaibweza
pa mutu pao, ati Ambuye Yehova.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Ohola ndi Oholiba acigololowo

1Ndipo anandidzera mau a Yehova, akuti, 2Wobadwa ndi munthu
iwe, panali akazi awiri, mai wao ndi mmodzi; 3ndipo anacita
cigololo iwo m'Aigupto, anacita cigololo m'ubwana wao; pomwepo
anthu anasindikiza maere ao, pomweponso anakhudza nsonga za
maere za unamwali wao. 4Ndipo maina ao ndiwo Ohola wamkuru,
ndi Oholiba mng'ono wace; nakhala anga, nabala ana amuna ndi
akazi. Ndipo maina ao, Samariya ndiye Ohola, ndi Yerusalemu
ndiye Oholiba. 5Koma Ohola anacita cigololo pamene anali wanga,
anaumirira mabwenzi ace Aasuri oyandikizana naye; 6obvala
cibakuwa, ziwanga, ndi akazembe, onsewo anyamata ofunika,
anthu oyenda pa akavalo. 7Ndipo anacita nao zigololo zace, ndiwo
anthu osankhika a ku Asuri onsewo, ndipo ali onse anawaumirira
anadziipsa nao mafano ao. 8Sanalekanso zigololo zace zocokera ku
Aigupto, pakuti anagona naye m'unamwali wace, nakhudza maere
a unamwali wace, namtsanulira cigololo cao. 9Cifukwa cace
ndampereka m'dzanja la mabwenzi ace, m'dzanja la Aasuri amene
anawaumirira. 10Iwowa anabvula umarisece wace, anatenga ana
ace amuna ndi akazi, namupha iyeyu ndi lupanga; ndi dzina lace
linamveka mwa akazi atamcitira maweruzo. 11Pamene mng'ono
wace Oholiba anaciona, anabvunda ndi kuumirira kwace koposa
iyeyo; ndi zigololo zace zidaposa zigololo za mkuru
wace. 12Anaumirira Aasuri, ziwanga, ndi akazembe oyandikizana
naye, obvala zangwiro, anthu oyenda pa akavalo, onsewo
anyamata ofunika. 13Ndipo ndinamuona kuti anadetsedwa, onse
awiri adatenga njira yomweyi. 14Ndipo anaonjeza zigololo zace,
naona amuna olembedwa pakhoma, zithunzithunzi za Akasidi
olembedwa ndi kundwe; 15omangira malamba m'cuuno mwao, ndi
nduwira zazikuru zonika pamitu pao, maonekedwe ao ngati
akalonga onsewo, akunga a ku Babulo, dziko la kubadwa kwao ndi
Kasidi. 16Ndipo pakuwaona anawalakalaka, nawatumira mithenga
ku dziko la Akasidi. 17Namdzera a ku Babulo ku kama wa cikondi,
namdetsa ndi cigololo cao, iyenso anadetsedwa nao; atatero moyo
wace unafukidwa nao. 18M'mwemo iye anaulula cigololo cace,
nabvula umarisece wace; pamenepo moyo wanga unaipidwa naye,
monga umo moyo unaipidwira mkuru wace. 19Koma anacurukitsa
zigololo zace, nakumbukila masiku a ubwana wace, muja anacita
cigololo m'dziko la Aigupto. 20Ndipo anaumirira amuna ao amene
nyama yao ikunga ya aburu, ndi kutentha kwao ngati kutentha kwa
akavalo. 21Momwemo wautsanso coipa ca ubwana wako,
pakukhudza Aaigupto nsonga za maere ako, cifukwa ca maere a
ubwana wako.

22Cifukwa cace, Oholiba, atero Ambuye Yehova, Taona
ndidzakuutsira mabwenzi ako amene moyo wako wakufidwa nao,
ndi kukufikitsira iwowa pozungulira ponse atsutsane nawe, 23a ku
Babulo, ndi Akasidi, Pekodi, ndi Sowa, ndi Kowa, ndi Aasuri onse
pamodzi nao, anyamata ofunika, ziwanga ndi akazembe onsewo,
akalonga ndi mandoda onsewo, oyenda ndi akavalo. 24Ndipo
adzakudzera ndi zida, magareta a nkhondo, ndi magareta ena,
pamodzi ndi msonkhano wa mitundu ya anthu; adzadziikira
pozungulira pako ndi zikopa zocinjiriza ndi zisoti; ndipo
ndidzawaika aweruze, nadzakuweruza monga mwa maweruzo
ao. 25Ndipo ndidzakuikira nsanje yanga, nadzakucitira mwaukali,
iwowa adzakudula mphuno ndi makutu; ndi otsiriza ako adzagwa
ndi lupanga, adzakucotsera ana ako amuna ndi akazi, ndi otsirizira
ako adzatha ndi moto. 26Adzakubvulanso zobvala zako, ndi
kukucotsera zokometsera zako zokongola. 27Motero
ndidzakuleketsera coipa cako, ndi cigololo cako cocokera m'dziko
la Aigupto; ndipo sudzazikwezeranso maso ako, kapena
kukumbukiranso Aigupto, 28Pakuti atero Ambuye Yehova, Taona
ndidzakupereka m'dzanja la iwo amene uwada, m'dzanja la iwo
amene moyo wako ufukidwa nao; 29ndipo adzacita nawe
mwaudani, nadzalanda zonse udazigwirira nchito, nadzakusiya
wamarisece ndi wausiwa; ndi umarisece wa zigololo zako
udzabvulidwa, dama lako ndi zigololo zako zomwe. 30Izi
adzakucitira cifukwa watsata amitundu, ndi kucita nao cigololo,
popezanso wadetsedwa ndi mafano ao. 31Wayenda m'njira ya
mkuru wako, cifukwa cace ndidzapereka cikho cace m'dzanja
lako. 32Atero Ambuye Yehova, M'cikho ca mkuru wako
udzamweramo ndico cacikuru ngati mcenje; adzakuseka
pwepwete, nadzakunyoza muli zambiri m'menemo. 33Udzadzala
ndi kuledzera ndi cisoni, ndi cikho codabwitsa ndi ca cipasuko, ndi
cikho ca mkuru wako Samariya. 34Udzamwa ici ndi kugugudiza, ndi
kuceceta-ceceta zibade zace, ndi kung'amba maere ako; pakuti
ndacinena, ati Ambuye Yehova. 35Cifukwa cace atero Ambuye
Yehova, Popeza wandiiwala Ine, ndi kunditaya pambuyo pako,
uzisenza iwenso coipa cako ndi zigololo zako.
36Ndipo Yehova anati kwa ine, Wobadwa ndi munthu iwe, kodi
udzaweruza Ohola ndi Oholiba? uwafotokozere tsono zonyansa
zao. 37Pakuti anacita cigololo, ndi m'manja mwao muli mwazi,
ndipo anacita cigololo ndi mafano ao, nawapititsiranso pamoto ana
ao amuna amene anandibalira, kuti athedwe. 38Anandicitiranso ici,
anadetsa malo anga opatulika tsiku lomwelo naipsa masabata
anga; 39pakuti ataphera mafano ao, ana ao analowa tsiku lomwelo
m'malo anga opatulika kuwadetsa; ndipo taona, anatero m'kati
mwa nyumba yanga. 40Ndiponso munatuma kuitana anthu ocokera

kutali, ndiwo munawatumira mthenga; ndipo taona, anadza amenewo unasamba, cifukwa ca iwo unapaka maso ako mankhwala, ndi kubvala zokometsera; 41ndipo unakhala pa kama waulemu, pali gome lokonzekeratu patsogolo pace; pamenepo unaika cofukiza conga ndi mafuta anga. 42Ndipo phokoso lalikuru lidaleka pomwepo, ndipo pamodzi ndi anthu wamba anabwera nao alodzera ocokera kucipululu, naika makoza m'manja mwa awiriwo, ndi akorona okongola pamitu pao. 43Pamenepo ndinati za uyu anakalamba nazo zigololo, Tsopano iwo adzacita zigololo naye, ndi iyenso nao. 44Ndipo analowa kwa iye monga umo amalowera kwa mkazi wacigololo, motero analowa kwa Ohola ndi Oholiba akazi oipawo. 45Ndipo anthu olungama adzawaweruza monga mwa maweruzo a acigololo, ndi maweruzo a akazi okhetsa mwazi; pakuti ndiwo acigololo, ndi m'manja mwao muli mwazi. 46Pakuti atero Ambuye Yehova, Ndidzawakweretsera msonkhano wa anthu, ndi kuwapereka awazunze, ndi kulanda cuma cao. 47Ndi msonkhanowo udzawaponya miyala, ndi kuwatha ndi malupanga ao, adzawapha ana ao amuna ndi akazi, ndi kutentha nyumba zao ndi moto. 48Momwemo ndidzaleketsa dama m'dzikomo, kuti alangizidwe akazi onse kusacita monga mwa dama lanu. 49Ndipo adzakubwezerani dama lanu, nimudzasenza macimo a mafano anu; motero mudzadziwa kuti Ine ndine Ambuye Yehova.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Fanizo la mphika wobwadamuka

1Anandidzeranso mau a Yehova caka cacisanu ndi cinai, mwezi
wakhumi, tsiku lakhumi la mwezi, ndi kuti, 2Wobadwa ndi munthu
iwe, Udzilembere dzina la tsiku lomwe lino, mfumu ya ku Babulo
wayandikira Yerusalemu tsiku lomwe lino. 3Ndipo uphere nyumba
yopandukayo fanizo, nunene nao, Atero Ambuye Yehova, Tereka
mphika; uutereke, nuthire madzi m'menemo. 4Longamo pamodzi
ziwalo zace, ziwalo zonse zokoma, mwendo wathako ndi
wamwamba; uudzaze ndi mafupa osankhika. 5Tengako coweta
cosankhika, nuikire mafupa mulu wa nkhuni pansi; ubwadamuke,
ndi mafupa ace omwe uwaphike m'mwemo. 6Cifukwa cace atero
Ambuye Yehova, Tsoka mudzi wokhetsa mwazi, mphika m'mene
muli dzimbiri, losaucokera dzimbiri lace; ucotsemo ciwalo ciwalo;
sanaugwera maere. 7Pakuti mwazi wace uli m'kati mwace anauika
pathanthwe poyera, sanautsanulira panthaka kuukwirira ndi
pfumbi. 8Pofuna kuutsa ukali, ndi kubwezera cilango, ndaika mwazi
wace pathanthwe poyera, kuti usakwiririke. 9Cifukwa cace atero
Ambuye Yehova, Tsoka mudzi wokhetsa mwazi, ndidzakulitsa mulu
wa nkhuni. 10Zicuruke nkhuni, kuleza moto, nyama ipse, uwiritse
msuzi wace, ubwadamuke, ndi mafupa ace atibuke. 11Pamenepo
uukhazike pa makara ace opanda kanthu m'menemo, kuti utenthe,
nuyake mkuwa wace; ndi kuti codetsa cace cisungunuke
m'mwemo, kuti dzimbiri lace lithe. 12Nchito ya mphika ndi
yolemetsa, koma dzimbiri lace lalikuru siliucokera, dzimbiri lace
liyenera kumoto. 13M'codetsa cako muli dama, popeza
ndinakuyeretsa; koma sunayeretsedwa, sudzayeretsedwanso
kukucotsera codetsa cako, mpaka nditakwaniritsa ukali wanga pa
iwe. 14Ine Yehova ndacinena, cidzacitika; ndipo ndidzacicita,
sindidzamasula, kapena kulekerera, kapena kuwaleka, monga mwa
njira zako, ndi monga umo unacitira adzakuweruza iwe, ati
Ambuye Yehova.

Kumwalira kwa mkazi wa Ezekieli kuli cizindikilo ca kwa Yuda

15Mau a Yehova anandidzeranso, akuti, 16Wobadwa ndi munthu
iwe, taona, ndikucotsera cokonda maso ako ndi cikomo, koma
usamve cisoni, kapena kulira, kapena kudza misozi. 17Usa moyo
mosamveka, usalira wakufayo, dzimangire cilemba, nubvale
nsapato ku mapazi ako, usaphimbe milomo yako, kapena kudya
mkate wa anthu. 18Ndipo nditalankhula ndi anthu m'mawa,
madzulo ace mkazi wanga anamwalira; ndi m'mawa mwace
ndinacita monga anandilamulira. 19Nanena nane anthu,
Simudzatiuza kodi zitani nafe izi muzicita? 20Ndipo ndinanena nao,
Anandidzera mau a Yehova, akuti, 21Nena ndi nyumba ya Israyeli,

Atero Ambuye Yehova, Taona, ndidzadetsa malo anga opatulika, ulemerero wa mphamvu yanu, cokonda m'maso mwanu, cimene moyo wanu ali naco cifundo; ndipo ana anu amuna ndi akazi otsalira inu adzagwa ndi lupanga. 22Ndipo mudzacita monga umo ndacitira ine, osaphimba milomo yanu, kapena kudya mkate wa anthu. 23Ndi zilemba zanu zidzakhala pamitu panu, ndi nsapato zanu ku mapazi anu, simudzacita cisoni kapena kulira, koma mudzaonda ndi mphulupulu zanu, ndi kubulirana wina ndi mnzace. 24Momwemo Ezekieli adzakhala kwa inu cizindikilo; umo monse anacitira iye mudzacita ndinu; cikadza ici mudzadziwa kuti Ine ndine Ambuye Yehova.
25Ndipo wobadwa ndi munthu iwe, sikudzakhala kodi tsiku loti ndiwacotsera mphamvu yao, cimwemwe cao copambana, cowakonda m'maso mwao, ndi cokhumbitsa mtima wao, ana ao amuna ndi akazi, 26kuti tsiku lomwelo wopulumukayo adzakudzera, kukumvetsa m'makutu mwako? 27Tsiku lomwelo pakamwa pako padzatsegukira wopulumukayo; mudzalankhula osakhalanso cete, momwemo udzawakhalira cizindikilo; ndipo adzadziwa kuti ine ndine Yehova.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Aneneratu za kulangidwa kwa Aamoni

1Ndipo mau a Yehova anandidzera, akuti, 2Wobadwa ndi munthu
iwe, Lozetsa nkhope yako kwa ana a Amoni, nuwanenere; 3nunene
kwa ana a Amoni, Tamverani mau a Ambuye Yehova, Atero
Ambuye Yehova, Popeza unati, Onyo, kunena malo anga opatulika;
muja anadetsedwa ndi kunena dziko la Israyeli; muja linapasuka
ndi kunena nyumba ya Yuda; muja adalowa kundende; 4cifukwa
cace taona, ndidzakupereka kwa ana a kum'mawa ukhale wao
wao, kuti amange misasa yao mwa iwe, namange pokhala pao
mwa iwe, iwo adzadya zipatso zako ndi kumwa mkaka
wako. 5Ndipo ndidzayesa Raba khola la ngamira, ndi ana a Amoni
popumula zoweta zazing'ono; matero mudzadziwa kuti Ine ndine
Yehova. 6Pakuti atero Ambuye Yehova, Waomba manja, ndi
kubvina, ndi kukondwera ndi cipeputso conse ca moyo wako,
kupeputsa dziko la Israyeli, 7cikufwa cace taona, ndakutambasulira
dzanja langa, ndipo ndidzakupereka ukhale cofunkha ca amitundu,
ndi kukudula mwa mitundu ya anthu, ndi kukutayikitsa m'maiko,
ndidzakuononga; motero udzadziwa kuti Ine ndine Yehova.

Za kulangidwa kwa Moabu

8Atero Ambuye Yehova, Popeza Moabu ndi Seiri akuti, Taona
nyumba ya Yuda ikunga amitundu onse; 9cifukwa cace taona,
ndidzatsegula pambali pace pa Moabu kuyambira ku midzi, ku
midzi yace yokhala mphepete, yokometsetsa ya m'dziko,
Betiyesimoti, Baalameoni, ndi Kiriataimu, 10kuwapereka kwa ana a
kum'mawa pamodzi ndi ana a Amoni; ndipo ndidzawapereka
akhale ao ao, kuti ana a Amoni asakumbukikenso mwa
amitundu; 11ndipo ndidzakwaniritsa maweruzo m'Moabu; motero
adzadziwa kuti Ine ndine Yehova.

Za kulangidwa kwa Edomu

12Atero Ambuye Yehova, Popeza Edomu anacita mobwezera
cilango pa nyumba ya Yuda, naparamula kwakukuru pakuibwezera
cilango, 13cifukwa cace atero Ambuye Yehova, Ndidzatambasulira
Edomu dzanja langa, ndi kulilikhira munthu ndi nyama, ndi
kulisandutsa labwinja; kuyambira ku Temani mpaka Dedani
adzagwa ndi lupanga. 14Ndipo ndidzalibwezera Edomu cilango
mwa dzanja la anthu anga Israyeli; ndipo adzacita m'Edomu
monga mwa mkwiyo wanga, ndi ukali wanga; motero adzadziwa
kubwezera cilango kwanga, ati Ambuye Yehova.

Za kulangidwa kwa Afilisti

15Atero Ambuye Yehova, Popeza Afilisti anacita mobwezera cilango
nabwezera cilango ndi mtima wopeputsa kuononga, ndi udani
wosatha, 16cifukwa cace atero Ambuye Yehova, Taona
ndidzatambasulira Afilisti dzanja langa, ndi kulikha. Akereti, ndi

kuononga otsalira mphepete mwa nyanja. 17Ndipo
ndidzawabwezera cilango cacikuru, ndi malango ankharwe; motero
adzadziwa kuti Ine ndine Yehova, pakuwabwezera cilango Ine.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Za kulangidwa kwa Turo

1Ndipo kunali caka cakhumi ndi cimodzi, tsiku loyamba la mwezi,
anandidzera mau a Yehova, akuti, 2Wobadwa ndi munthu iwe,
popeza Turo ananyodola Yerusalemu, ndi kuti, Onyo, watyoka uwu
udali cipata ca mitundu ya anthu; wanditembenukira ine;
ndidzakhuta ine, wapasuka uwu; 3cifukwa cace atero Ambuye
Yehova, Taona ndikutsutsa iwe, Turo, ndidzakukweretsera
amitundu, monga nyanja iutsa mafunde ace. 4Ndipo adzagumula
malinga a Turo, ndi kugwetsa nsanja zace; inde ndidzausesa
pfumbi lace, ndi kuuyesa pathanthwe poyera. 5Udzakhala poyanika
khokapakati pa nyanja, pakuti Ine ndacinena, ati Ambuye Yehova;
ndipo udzakhala cofunkha ca amitundu. 6Ndi ana ace akazi okhala
kumunda adzaphedwa ndi lupanga; motero adzadziwa kuti Ine
ndine Yehova. 7Pakuti atero Ambuye Yehova, Taona ndidzafikitsira
Turo Nebukadirezara mfumu ya ku Babulo, mfumu ya mafumu,
yocokera kumpoto ndi akavalo, ndi magareta, ndi apakavalo, ndi
msonkhano wa anthu ambiri. 8Ana ako akazi adzawapha kumunda
ndi lupanga; ndipo adzakumangira nsanja, ndi kukuundira
mtumbira, ndi kukuimikira cikopa. 9Nadzaikira malinga ako
zogumulira, nadzagwetsa nsanja zako ndi zida zace. 10Papeza
acuruka akavalo ace, pfumbi lao lidzakukuta; malinga ako
adzagwedezeka ndi phokoso la apakavalo, ndi njinga za magareta,
palowa iye pa zipata zako, monga umo amalowera m'mudzi
popasukira linga lace. 11Ndi ziboda za akavalo ace iye
adzapondaponda m'makwalala ako onse; adzapha anthu ako ndi
lupanga; ndi zoimiritsa za mphamvu yako zidzagwa pansi. 12Ndipo
adzalanda cuma cako ndi kufunkha malonda ako, nadzagwetsa
malinga ako ndi kupasula nyumba zako zofunika, nadzaponya
miyala yako, ndi mitengo yako, ndi pfumbi lako, m'madzi. 13Ndipo
ndidzaleketsa phokoso la nyimbo zako, ndi kulira kwa mazeze ako
sikudzamvekanso. 14Ndipo ndidzakuyesa pathanthwe poyera;
udzakhala poyanika khoka, sadzakumanganso; pakuti Ine Yehova
ndacinena, ati Ambuye Yehova.
15Atero Ambuye Yehova kwa Turo, Zisumbu sizidzagwedezeka
nanga pomveka kugwa kwako, pabuula olasidwa, pakucitika
kuphako pakati pako? 16Pamenepo akalonga onse a kunyanja
adzatsika ku mipando yacifumu yao, nadzabvula zobvala zao
zopikapika, nadzabvala kunjenjemera, nadzakhala panthaka pansi,
nadzanjenjemera mphindi zonse ndi kukudabwa. 17Ndipo
adzakukwezera nyimbo ya maliro, ndi kunena nawe, Watayika
bwanji, ndiwe pakhala pa anthu a panyanja, mudzi womveka,
unalimbika panyanja, uwo ndi okhalamo, amene anakhalitsa
kuopsa kwao pa onse okhala momwemo! 18Pamenepo zisumbu

zidzanjenjemera tsiku la kugwa kwako, inde zisumbu za kunyanja
zidzatenga nkhawa pa kucokera kwako. 19Pakuti atero Ambuye
Yehova, Pamene ndikusandutsa mudzi wapasuka, ngati midzi
yosakhalamo anthu, ndi kukukweretsera nyanja, nadzakumiza
madzi akuru; 20pamenepo ndidzakutsitsa nao otsikira kumanda,
kwa anthu a kale lomwe, ndi kukukhalitsa ku malo a kunsi kwa
dziko, kopasukira kale lomwe, pamodzi nao otsikira kumanda, kuti
mwa iwe musakhale anthu; ndipo ndidzaika ulemerero m'dziko la
amoyo, 21ndidzakuika woopsa; ndipo sudzaonekanso, cinkana
akufunafuna sudzapezekanso konse, ati Ambuye Yehova.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Nyimbo ya maliro ya pa Turo

1Anandidzeranso mau a Yehova, akuti, 2Ndipo iwe wobadwa ndi
munthu, Takwezera Turo nyimbo ya maliro; 3nuti kwa Turo, Iwe
wakukhala polowera m'nyanja, wakucita malonda ndi mitundu ya
anthu m'zisumbu zambiri, atero Ambuye Yehova, Iwe, Turo, wati,
Ine ndine wokongola wangwiro. 4M'mphepete mwako muli m'kati
mwa nyanja, iwo anakumanga iwe anakonza kukongola kwako
kukhale kwangwiro. 5Anaceka matabwa ako onse amlombwa wa ku
Seniri, anatenga mikungudza ya ku Lebano kukupangira
milongoti. 6Anasema nkhafi zako za thundu wa ku Basana,
anapanga mipando yako yamnyanga, woika mu mtengo wanaphini
wocokera ku zisumbu za Kitimu. 7Thanga lako ndi labafuta
wopikapika wa ku Aigupto, likhale ngati mbendera yako; cophimba
cako ndico nsaru yamadzi ndi yofiirira zocokera ku zisumbu za
Elisa. 8Okhala m'Zidoni ndi Arivadi ndiwo opalasa ako; anzeru ako,
Turo, okhala mwa iwe, ndiwo oongolera ako. 9Akr-ru a ku Gebala
ndi eni luso ace anali mwa iwe kukonza ziboo zako; zombo zonse
za kunyanja pamodzi ndi amarinyero ao anali mwa iwe kusinthana
nawe malonda. 10Aperisiya, Aludi, Apuri, anali m'khamu lako;
anthu ako a nkhondo anapacika cikopa ndi cisoti mwa iwe,
anamveketsa kukoma kwako. 11Anthu a Ativadi pamodzi ndi
ankhondo ako anali pa malinga ako pozungulira, ndi Agamadi anali
mu nsanja zako; anapacika zikopa zao pa makoma ako
pozungulira, anakwaniritsa kukoma kwako. 12Tarisi anagulana
nawe malonda m'kucuruka kwa cuma ciri conse; anagula malonda
ako ndi siliva ndi citsulo, seta ndi ntobvu. 13Yavani, Tuba, Meseke,
anagulana nawe malonda; ndi anthu amoyo ndi zotengera
zamkuwa anagulana nawe malonda. 14Iwo a nyumba ya Togarima
anagula malonda ako ndi akavalo, ndi akavalo a nkhondo, ndi
nyuru. 15Anthu a ku Dedani anakutsatsa malonda, zisumbu zambiri
zinazolowerana nawe malonda ako, anabwera nazo minyanga ndi
phingo kugulana nawe malonda. 16Aramu anacita nawe malonda
cifukwa ca zambirizo udazipanga, anagula malonda ako ndi
smaragido, nsaru yofiirira, ndi yopikapika, ndi bafuta, ndi korale,
ndi ngale. 17Yuda ndi dziko la Israyeli anagulana nawe malonda,
anagula malonda ako ndi tirigu wa ku Miniti, ndi zozuna, ndi uci,
ndi mafuta, ndi mafuta amankhwala. 18Damasiko anagulana nawe
malonda cifukwa ca zambirizo udazipanga, cifukwa ca kucuruka
kwa cuma ciri conse, ndi vinyo wa ku Keliboni, ndi ubweya wa
nkhosa woyera. 19Vedani ndi Yavani anagula malonda ako ndi
thonje, unagulana nao citsulo cosalala, ngaho, ndi
mzimbe. 20Dedani anagulana nawe malonda ndi nsaru za mtengo
wace zoyenda nazo pa kavalo. 21Arabu ndi akalonga onse a ku

Kedara anazolowerana nao malonda ako; ana a nkhosa, nkhosa
zamphongo, ndi mbuzi, izi anagulana nawe. 22Amalonda a ku Seba
ndi a ku Rama anagulana nawe malonda; anagula malonda ako ndi
zonunkhira zoposa ziri zonse, ndi miyala iri yonse ya mtengo wace,
ndi golidi. 23Harani ndi Kane ndi Edene, amalonda a ku Seba Asuri
ndi Kilimadi, anagulana nawe malonda. 24Awa anagulana nawe
malonda ndi zobvala zosankhika, ndi mitumba ya nsaru zofiirira
ndi zopikapika, ndi cuma ca thonje lopotapota, ndi zingwe zopota
zolimba za malonda ako. 25Zombo za ku Tarisi ndizo amtengatenga
a malonda ako; ndipo unadzazidwa ndi cuma ndi ulemu waukuru
pakati pa nyanja, 26Opalasa ako anakufikitsa ku madzi akuru;
mphepo ya kum'mawa inakutyola m'kati mwa nyanja, 27Cuma
cako, zako zogulana nazo malonda ako, amarinyero ako, ndi
oongolera ako, amisiri ako, ndi ogulitsa malonda ako, ndi ankhondo
ako onse okhala mwa iwe, pamodzi ndi msonkhano wonse uli
pakati pa iwe, adzagwa m'kati mwa nyanja tsiku la kugwa
kwako. 28Pakumveka mpfuu wa oongolera ako mabwalo ako
adzagwedezeka. 29Ndi onse ogwira nkhafi, amarinyero, ndi
oongolera onse a kunyanja, adzatsika ku zombo zao, nadzaima
pamtunda, 30nadzamveketsa mau ao pa iwe, nadzalira mowawa
mtima, nadzathira pfumbi pamitu pao, nadzakunkhulira
m'maphulusa, 31nadzameta mpala, cifukwa ca iwe,
nadzadzimangira ziguduli m'cuuno, nadzakulirira ndi mtima
wowawa maliro owawa. 32Ndipo pakulira adzakukwezera nyimbo
ya maliro, ndi kukulirira, ndi kuti, Wakunga Turo ndani, wakunga
uyu waonongeka pakati pa nyanja? 33Pakuturuka malonda ako
m'nyanja unadzaza mitundu yambiri ya anthu, unalemeretsa
mafumu a pa dziko lapansi ndi cuma cako cocuruka ndi malonda
ako. 34Muja unatyoka ndi nyanja m'madzi akuya malonda ako ndi
msonkhano wako wonse adagwa pakati pako. 35Onse okhala pa
zisumbu adagwa nawe, ndi mafumu ao aopsedwa kwambiri
zikhululuka nkhope zao. 36Amalonda mwa mitundu ya anthu
akunyodola, wakhala coopsetsa iwe, ndipo sudzakhalanso konse.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Aneneratu za kulangidwa kwa mfumu ya ku Turo

1Ndipo anandidzera mau a Yehova, akuti, 2Wobadwa ndi munthu
iwe, uziti kwa kalonga wa Turo, Atero Ambuye Yehova, Popeza
mtima wako wadzikweza, nuti, Ine ndine mulungu, ndikhala pa
mpando wa Mulungu pakati pa nyanja, ungakhale uli munthu,
wosati Mulungu, ungakhale waika mtima wako ngati mtima wa
Mulungu, 3taona, ndiwe wanzeru woposa Danieli, palibe cinsinsi
angakubisire; 4mwa nzeru zako ndi luntha lako wadzionerera
cuma, wadzionereranso golidi ndi siliva mwa cuma cako; 5mwa
nzeru zako zazikuru ndi kugulana malonda kwako wacurukitsa
cuma cako, ndi mtima wako wadzikuza cifukwa ca cuma
cako; 6cifukwa cace atero Ambuye Yehova, Popeza waika mtima
wako ngati mtima wa Mulungu; 7cifukwa cace taona,
ndidzakufikitsira alendo oopsa a mitundu ya anthu, iwo
adzasololera malupanga ao nzeru zako zokongola, nadzaipsa
kunyezimira kwako. 8Adzakutsitsira kumanda, nudzafa mafedwe a
ophedwa m'kati mwa nyanja. 9Kodi udzanena ndithu pamaso pa
iye wakupha iwe, Ine ndine Mulungu, pokhala uli munthu, wosati
Mulungu, m'dzanja la iye wakupha iwe. 10Udzafa mafedwe a
osadulidwa ndi dzanja la alendo, pakuti ndacinena, ati Ambuye
Yehova.

Nyimbo ya maliro yolirira mfumu ya Turo

11Nandidzeranso mau a Yehova, akuti, 12Wobadwa ndi munthu iwe,
kweza nyimbo ya maliro yolirira mfumu ya Turo, nuziti kwa iye,
Atero Ambuye Yehova, Wakomera muyeso ndi cizindikilo, wodzala
ndi nzeru wokongola wangwiro. 13Unali m'Edene, munda wa
Mulungu, mwala uli wonse wa mtengo wace unali copfunda cako,
sardiyo, topazi, diamondi, berulo, sohamu, ndi yaspi, safiro, nofeki,
bareketi, ndi golidi; malingaka ako ndi akazi ako anakutumikira
tsiku lolengedwa iwe zinakonzekeratu. 14Unali kerubi wodzozedwa
wakuphimba, ndipo ndinakuika unali pa phiri lopatulika la Mulungu,
anayendayenda pakati pa miyala yamoto. 15Unali wangwiro m'njira
zako cilengedwere iwe, mpaka cinapezeka mwa iwe
cosalungama. 16Mwa kucuruka kwa malonda ako anakudzaza
m'kati mwako ndi ciwawa, ndipo unacimwa; cifukwa cace
ndinakukankha kukucotsa pa phiri la Mulungu; ndipo
ndinakuononga, kerubi wakuphimba iwe, kukucotsa pakati pa
miyala yamoto. 17Unadzikuza mtima cifukwa ca kukongola kwako,
waipsa nzeru zako; cifukwa ca kuwala kwako ndakugwetsa pansi,
ndakuika pamaso pa mafumu, kuti akupenye. 18Mwa mphulupulu
zako zocuruka ndi malonda ako osalungama waipsa malo ako
opatulika; cifukwa cace ndaturutsa moto m'kati mwako
wakunyeketsa iwe; ndipo ndakusandutsa mapulusa panthaka

pamaso pa onse akuona. 19Onse akudziwa iwe mwa mitundu ya
anthu adzadabwa nawe; wasanduka coopsa, ndipo sudzakhalanso
konse.

Za kulangidwa kwa Zidoni

20Anandidzeranso mau a Yehova, akuti, 21Wobadwa ndi munthu
iwe, lozetsa nkhope yako ku Zidoni, nuunenere; 22uziti, Atero
Ambuye Yehova, Taona, nditsutsana nawe Zidoni, ndipo
ndidzalemekezedwa pakati pako; ndipo adzadziwa kuti Ine ndine
Yehova pakucita Ine maweruzo mwa uwu, ndi kuzindikiridwa
Woyera mwa uwu. 23Pakuti ndidzatumiza mliri ndi mwazi ilowe
m'makwalala ace, ndi olasidwa adzagwa m'kati mwace ndi lupanga
lougwera pozungulira ponse; motero adzadziwa kuti Ine ndine
Yehova. 24Ndipo nyumba ya Israyeli siidzakhalanso nayo mitungwi
yolasa, kapena minga yaululu ya ali yense wakuizinga ndi
kuipeputsa; motero adzadziwa kuti Ine ndine Ambuye Yehova.
25Atero Ambuye Yehova, Pakusonkhanitsa nyumba ya Israyeli mwa
mitundu ya anthu anabalalikamo, ndidzazindikirika Woyera mwa
iwowa, pamaso pa amitundu; ndipo adzakhala m'dziko mwao
mwao ndinalipereka kwa Yakobo mtumiki wanga. 26Nadzakhalamo
osatekeseka, nadzamanga nyumba, ndi kunka mpesa m'mindamo,
nadzakhalamo mosatekeseka, ndikatha kukwaniritsira maweruzo
pa onse akuwapeputsa pozungulira pao; motero adzadziwa kuti Ine
ndine Yehova Mulungu wao.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Aneneratu za kulangidwa kwa Aigupto

1Caka cakhumi, mwezi wakhumi, tsiku lakhumi ndi ciwiri la
mweziwo, anandidzera mau a Yehova, akuti, 2Wobadwa ndi
munthu iwe, lozetsa: nkhope yako itsutsane naye Farao mfumu ya
Aigupto, nunenere motsutsana ndi iye, ndi Aigupto lonse; 3nena,
uziti, Atero Ambuye Yehova, Taona nditsutsana nawe, Farao mfumu
ya Aigupto, ng'ona yaikuru yakugona m'kati mwa mitsinje yace,
imene ikuti, Mtsinje wanga ndi wangatu, ndadzipangira ndekha
uwu. 4Koma ndidzaika mbedza m'kamwa mwako, ndi
kumamatiritsa nsomba za m'mitsinje mwako ku mamba ako; ndipo
ndidzakukweza kukuturutsa m'kati mwa mitsinje yako, pamodzi ndi
nsomba zonse za m'mitsinje mwako zomamatira pa mamba
ako. 5Ndipo ndidzakutaya kucipululu, iwe ndi nsomba zonse za
m'mitsinje mwako; udzagwa kuthengo koyera, sudzaunjikidwa,
kapena kuoledwa; ndakupereka ukhale cakudya ca zirombo za
padziko, ndi mbalame za kumlengalenga, 6Ndi onse okhala
m'Aigupto adzadziwa kuti Ine ndine Yehova, popeza anakhalira
nyumba ya Israyeli mcirikizo wabango. 7Muja anakugwira ndi
dzanja unatyoka, ndi kulasa mapewa ao onse; ndi muja
anakutsamira unatyoka, ndi kuwagwedeza ziuno zao
zonse. 8Cifukwa cace atero Ambuye Yehova, Taona, ndikudzera ndi
lupanga, ndi kukulikhira munthu ndi nyama. 9Ndi dziko la Aigupto
lidzakhala lopasuka ndi labwinja; ndipo adzadziwa kuti Ine ndine
Yehova, popeza anati, Mtsinjewo ndi wanga, ndinaulenga
ndine. 10Cifukwa cace taona, nditsutsana ndi iwe ndi mitsinje yako,
ndipo ndidzasandutsa dziko la Aigupto likhale lopasuka konse, ndi
labwinja, kuyambira nsanja ya Sevene kufikira malire a
Kusi. 11Silidzapitamo phazi la munthu, kapena phazi la nyama
losapitamo, losakhalamo anthu zaka makumi anai. 12Ndipo
ndidzasandutsa dziko la Aigupto labwinja pakati pa maiko a
mabwinja; ndi midzi yace pakati pa midzi yopasuka idzakhala
yabwinja zaka makumi anai; ndipo ndidzamwaza Aaigupto mwa
amitundu, ndi kuwabalalitsa m'maiko. 13Pakuti atero Ambuye
Yehova, Zitatha zaka makumi anai ndidzasonkhanitsa Aaigupto ku
mitundu ya anthu kumene anamwazikirako; 14ndipo ndidzabweza
undende wa Aigupto, ndi kuwabwezera ku dziko la Patro, ku dziko
la kubadwa kwao, ndi komweko adzakhala ufumu
wopepuka, 15Udzakhala wopepuka wa maufumu onse,
sudzadzikwezanso pa amitundu; ndipo ndidzawacepsa, kuti
asacitenso ufumu pa amitundu. 16Ndipo sudzakhalanso cotama ca
nyumba ya Israyeli, kukumbutsa mphulupulu, pakuwatembenukira
kuwatsata; motero adzadziwa kuti Ine ndine Ambuye Yehova.

17Ndipo kunali caka ca makumi awiri mphambu zisanu ndi ziwiri
mwezi woyamba, tsiku loyamba la mwezi, anandidzera mau a
Yehova, akuti, 18Wobadwa ndi munthu iwe, Nebukadirezara mfumu
ya ku Babulo anacititsa ankhondo ace nchito yaikuru yoponyana
ndi Turo; mitu yonse inacita dazi, ndi mapewa onse ananyuka;
koma analibe kulandira mphotho ya ku Turo, iye kapena ankhondo
ace, pa nchito anagwirayo; 19cifukwa cace atero Ambuye Yehova,
Taona, ndidzapereka dziko la Aigupto kwa Nebukadirezara mfumu
ya ku Babulo; ndipo adzacoka nao aunyinji ace, nadzafunkha ndi
kulanda zace, ndizo mphotho ya khamu lace. 20Ndamninkha dziko
la Aigupto combwezera nchito yace, popeza anandigwirira nchito,
ati Ambuye Yehova.
21Tsiku ilo ndidzameretsera nyumba ya Israyeli nyanga; ndipo
ndidzakutsegulira pakamwa pakati pao; motero adzadziwa kuti Ine
ndine Yehova.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Aigupto adzagonjetsedwa ndi mfumu ya ku Babulo

1Anandidzeranso mau a Yehova, akuti, 2Wobadwa ndi munthu iwe,
nenera, uziti, Atero Ambuye Yehova, Liritsani, Ha, tsikulo 3Pakuti
layandikira tsiku, layandikira tsiku la Yehova, tsiku lamitambo,
ndiyo nyengo ya amitundu. 4Ndi lupanga lidzadzera Aigupto, ndi
m'Kusi mudzakhala kuwawa kwakukuru, pakugwa ophedwa
m'Aigupto; ndipo adzacotsa aunyinji ace, ndi maziko ace
adzagadamuka, 5Kusi, ndi Puti, ndi Ludi, ndi osokonezeka onse, ndi
Kubi, ndi anthu a dziko lopangana nao, adzagwa pamodzi nao ndi
lupanga.
6Atero Yehova, Iwonso ocirikiza Aigupto adzagwa, ndi mphamvu
yace yodzikuza idzatsika, kuyambira nsanja ya Sevene adzagwa
m'kati mwace ndi lupanga, ati Ambuye Yehova. 7Ndipo adzakhala
opasuka pakati pa maiko opasuka, ndi midzi yace idzakhala pakati
pa midzi yopasuka. 8Ndipo adzadziwa, kuti Ine ndine Yehova,
nditaika moto m'Aigupto, naonongeka onse akumthandiza. 9Tsiku
ilo mithenga idzaturuka pamaso panga m'zombo kuopsa Akusi
osalabadira; ndipo kudzakhala kuwawa kwakukuru pakati pao,
monga tsiku la Aigupto, pakuti taona, likudza.
10Atero Ambuye Yehova, Ndidzaleketsa kusokosera kwa Aigupto
ndi dzanja la Nebukadirezara mfumu ya ku Babulo. 11Iye ndi anthu
ace pamodzi naye, woopsa amitundu, adzatengedwa alikonge
dzikolo, nadzasololera Aigupto malupanga ao, ndi kudzaza dziko
ndi ophedwa. 12Ndipo ndidzaphwetsa mitsinje, ndi kugulira dziko
m'dzanja la anthu oipa, ndipo ndidzalisandutsa likhale dziko
lopasuka, ndi zonse ziri m'mwemo mwa dzanja la alendo; Ine
Yehova ndacinena.
13Atero Ambuye Yehova, Ndidzaonongansa mafano, ndi kuleketsa
milungu yopanda pace ku Nofu; ndipo sadzaonekanso kalonga
wocokera ku Aigupto, ndipo ndidzaopsa dziko la Aigupto. 14Ndipo
ndidzasandutsa Patro labwinja, ndi kuika moto m'Zoani, ndi
kukwaniritsa maweruzo m'No. 15Ndipo ndidzatsanulira ukali wanga
pa Sini, polimbika peni peni pa Aigupto, ndi kulikha aunyinji a
No. 16Ndipo ndidzaika moto m'Aigupto; Sini adzamva kuwawa
kwakukuru, ndi No adzagawika pakati, ndi Nofu adzaona adani
usana. 17Anyamata a Avene ndi Pibezeti adzagwa ndi lupanga, ndi
midziyi idzalowa undende. 18Ndi ku Tehafinehesi kudzada usana,
pakutyola Ine magoli a Aigupto komweko; ndi mphamvu yace
yodzikuza idzalekeka m'menemo; kunena za ilo mtambo
udzaliphimba, ndi ana ace akazi adzalowa undende. 19Motero
ndidzakwaniritsa maweruzo m'Aigupto, ndipo adzadziwa kuti Ine
ndine Yehova.

20Ndipo kunali caka cakhumi ndi cimodzi, mwezi woyamba, tsiku
lacisanu ndi ciwiri la mwezi, anandidzera mau a Yehova,
akuti, 21Wabadwa ndi munthu iwe, ndatyola dzanja la Parao mfumu
ya Aigupto, ndipo taona, silinamangidwa kuti lipole, kulikulunga ndi
nsaru, kulilimbitsa ligwire lupanga. 22Cifukwa cace atero Ambuye
Yehova, Taona, Ine ndilimbana naye Parao mfumu ya Aigupto,
ndidzatyola manja ace, lolimba ndi lotyokalo, ndi kutayitsa lupanga
m'dzanja lace. 23Ndipo ndidzamwaza Aaigupto mwa amitundu, ndi
kuwabalalitsa m'maiko. 24Ndipo ndidzalimbitsa manja a mfumu ya
ku Babulo, ndi kuika lupanga langa m'dzanja lace; koma
ndidzatyola manja a Parao, ndipo adzabuula pamaso pace
mabuulo a munthu wopyozedwa. 25Ndipo ndidzalimbitsa manja a
mfumu ya ku Babulo, koma manja a Parao adzagwa; ndipo
adzadziwa kuti Ine ndine Yehova pakuika Ine lupanga langa
m'dzanja la mfumu ya ku Babulo, nalitambasula Iye pa dziko la
Aigupto. 26Ndipo ndidzamwaza Aaigupto mwa amitundu, ndi
kuwabalalitsa mwa amitundu; motero adzadziwa kuti Ine ndine
Yehova.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Mau ena oneneratu za Farao

1Ndipo kunali caka cakhumi ndi cimodzi, mwezi wacitatu, tsiku
loyamba la mwezi, anandidzera mau a Yehova, akuti, 2Wobadwa
ndi munthu iwe, nena kwa Farao mfumu ya Aigupto ndi aunyinji
ace, Ufanana ndi yani m'ukulu wako? 3Taona, Asuri anali
mkungudza wa ku Lebano ndi nthambi zokoma zobvalira, wautali
msinkhu, kunsonga kwace ndi kumitambo. 4Madzi anaumeretsa,
cigumula cinaukulitsa, mitsinje yace inayenda, nizungulira munda
wace, nipititsa micera yace ku mitengo yonse ya
kuthengoko. 5Cifukwa cace msinkhu wace unaposa mitengo yonse
ya kuthengo, ndi nthambi zace zinacuruka, ndi nthawi zace
zinatalika, Cifukwa ca madzi ambiri pophuka uwu. 6Mbalame zonse
za m'mlengalenga zinamanga zisa zao pa nthambi zace, ndi pansi
pa nthawi zace zinaswana nyama zonse za kuthengo, ndi pa
mthunzi wace inakhala mitundu yonse yaikuru ya
anthu. 7M'mwemo unakoma m'ukulu wace, m'kutalika kwa nthawi
zace, popeza muzu wace unakhala ku madzi ambiri. 8Mikungudza
ya m'munda wa Mulungu siinathe kuubisa, milombwasimanga
nthambi zace, mifula siinanga nthawi zace; m'munda wa Mulungu
munalibe mtengo wofanana nao kukoma kwace. 9Ndinaupanga
wokoma ndi nthawi zace zocuruka; ndi mitengo yonse ya m'Edene
inali m'munda wa Mulungu inacita nao nsanje.
10Cifukwa cace atero Ambuye Yehova, Popeza mtengowo unakuza
msinkhu wace, nufikitsa nsonga yace kumitambo, nukwezeka
mtima wace m'kukula kwace, 11ndidzaupereka m'dzanja la
wamphamvu wa amitundu; iye adzacita naotu, Ine ndautaya mwa
coipa cace. 12Ndipo alendo oopsawo a amitundu anaulikhatu,
nausiya; nthawi zace zidagwa pamapiri ndi m'zigwa zonse, ndi
nthambi zace zinatyokera ku timitsinje tonse ta m'dziko; ndi
mitundu yonse ya anthu a pa dziko lapansi inatsika ku mthunzi
wace, niusiya. 13Pogwera pace padzakhala mbalame zonse za
m'mlengalenga, ndi nyama zonse za kuthengo zidzakhala pa
nthambi zace; 14kuti mitengo iri yonse ya kumadzi isadzikuze
cifukwa ca msinkhu wao, kapena kufikitsa nsonga zao pakati pa
mitambo, ndi kuti amphamvu ao asaime m'kukula kwao, ndiwo
onse akumwa madzi; pakuti onsewo aperekedwa ku imfa munsi
mwace mwa dziko, pakati pa ana a anthu, pamodzi ndi iwo otsikira
kumanda.
15Atero Ambuye Yehova, Tsiku lija anatsikira kumanda ndinacititsa
maliro, ndinamphimbira nyanja, ndinacepsa mitsinje yace, ndi
madzi akuru analetseka; ndipo ndinamdetsera Lebano, ndi
mitengo yonse ya kuthengo inafota cifukwa ca
uwo. 16Ndirtagwedeza amitundu ndi phokoso la kugwa kwace,

muja ndinamgwetsera kumanda, pamodzi ndi iwo otsikira kumanda; ndi mitengo yonse ya ku Edene yosankhika, ndi yokometsetsa ya ku Lebano, yonse yakumwa madzi, inasangalala munsi mwace mwa dziko lapansi. 17Iwonso anatsika naye kumanda kwa iwo ophedwa ndi lupanga, ndiwo amene adakhala dzanja lace okhala mumthunzi mwace pakati pa amitundu.
18Momwemo ufanana ndi yani m'ulemerero ndi ukulu pakati pa mitengo ya Edene? koma udzatsitsidwa pamodzi ndi mitengo ya Edene munsi mwace mwa dziko lapansi, udzagona pakati pa osaditiidwa, pamodzi ndi iwo ophedwa ndi lupanga. Uwu ndi Farao ndi aunyinji ace onse, ati Ambuye Yehova.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Nyimbo ya maliro ya pa Farao

1Ndipo kunali caka cakhumi ndi ciwiri, mwezi wakhumi ndi ciwiri,
tsiku loyamba la mwezi, anandidzera mau a Yehova,
akuti, 2Wobadwa ndi munthu iwe, takwezera Farao mfumu ya
Aigupto nyimbo yamaliro; uziti naye, Unafanana nao msona wa
mkango wa amitundu, unanga ng'ona ya m'nyanja, unabuka
m'mitsinje mwako, nubvundulira madzi ndi mapazi ako, ndi
kudetsa mitsinje yao. 3Atero Ambuye Yehova, Ndidzakuponyera
khoka langa mwa msonkhano wa mitundu yambiri ya anthu,
nadzakubvuulira m'khoka mwanga. 4Ndipo ndidzakusiya
pamtunda, ndidzakuponya kuthengo koyera, ndi kuteretsa pa iwe
mbalame zonse za m'mlengalenga, ndi kukhutitsa zirombe za
dziko lonse lapansi ndi iwe. 5Ndipo ndidzaika nyama yako
pamapiri, ndi kudzaza zigwa ndi msinkhu wako. 6Ndipo
ndidzamwetsa dziko losambiramo iwe ndi mwazi wako, kufikira
kumapiri; ndi mitsinje idzadzala nawe. 7Ndipo pakukuzima iwe
ndidzaphimba thambo, ndi kudetsa nye nyezi zace; ndidzaphimba
dzuwa ndi mtambo, ndi mwezi sudzaonetsa kuwala
kwace. 8Ndidzakudetsera miyuni ronse yakuunikira kuthambo, ndi
kucititsa mdima pa dziko lako, ati Ambuye
Yehova. 9Ndidzabvutanso mitima ya mitundu yambiri ya anthu,
pakufikitsa Ine cionongeko cako mwa amitundu, m'maiko amene
sunawadziwa. 10Ndipo ndidzasumwitsa nawe mitundu yambiri ya
anthu, ndi mafumu ao adzacita malunga cifukwa ca iwe,
pakung'animitsa Ine lupanga langa pamaso pao; ndipo
adzanjenjemera mphindi zonse, yense cifukwa ca moyo wace tsiku
lakugwa Iwe, 11Pakuti atero Ambuye Yehova, Lupanga la mfumu ya
ku Babulo lidzakudzera. 12Ndidzagwetsa aunyinji ako ndi
malupanga a eni mphamvu, ndiwo onse oopsetsa a amitundu;
ndipo adzaipsa kudzikuza kwa Aigupto, ndi aunyinji ace onse
adzaonongeka. 13Ndidzaononganso nyama zace zonse za ku madzi
ambiri; ndi phazi la munthu silidzabvundulira, ndi ziboda za nyama
zosawabvundulira. 14Pamenepo ndidzadikhitsa madzi ace, ndi
kuyendetsa madzi a m'mitsinje mwao ngati mafuta, ati Ambuye
Yehova. 15Pakusanduliza Ine dziko la Aigupto likhale lopasuka ndi
labwinja, dziko losowa zodzaza zace, pakukantha Ine onse okhala
m'mwemo, pamenepo adzadziwa kuti ine ndine Yehova. 16Iyi ndi
nyimbo ya maliro adzalira nayo, ana akazi a amitundu adzacita
nayo maliro; adzalirira nayo Aigupto ndi aunyinji ace onse, ati
Ambuye Yehova.

Mau a kulirira aunyinji a Aigupto

17Kunalinso caka cakhumi ndi ciwiri, tsiku lakhumi ndi cisanu la
mwezi, anandidzera mau a Yehova, ndi kuti, 18Wobadwa ndi

munthu iwe, lirira aunyinji a Aigupto, nuwagwetsere iye ndi ana akazi a amitundu omveka kunsi kwa dziko, pamodzi ndi iwo akutsikira kudzenje. 19Uposa yani m'kukoma kwako? tsika, nuikidwe ndi osadulidwa. 20Adzagwa pakati pa iwo ophedwa ndi lupanga, operekedwa kwa lupanga, mkokereko ndi aunyinji ace onse. 21Amphamvu oposa ali m'kati mwa manda adzanena naye, pamodzi ndi othandiza ace, Anatsikira, agonako osadulidwawo, ophedwa ndi lupanga, 22Asuri ali komwe ndi msonkhano wace wonse, manda ace amzinga; ophedwa onsewo, adagwa ndi lupanga; 23manda ao aikidwa ku malekezero a dzenje, ndi gulu lace lizinga manda ace; ophedwa onsewo adagwa ndi lupanga, amene anaopsetsa m'dziko la amoyo. 24Elamu ali komwe ndi gulu lace lonse lozinga manda ace; ophedwa onsewo, adagwa ndi lupanga; amene anatsikira osadulidwa kunsi kwace kwa dziko, amene anaopsetsa m'dziko la amoyo, nasenza manyazi ao, pamodzi ndi iwo akutsikira kudzenje. 25Pakati pa ophedwa anamuikira kama, iye ndi aunyinji ace onse, manda ace amzinga, onsewo osadulidwa, ophedwa ndi lupanga, pakuti anaopsetsa m'dziko la amoyo, nasenza manyazi ao, pamodzi ndi iwo akutsikira kudzenje, aikidwa pakati pa ophedwa, 26Meseke, Tubala, ndi aunyinji ace onse ali komweko, manda ace amzinga; onsewo osadulidwa, ophedwa ndi lupanga; pakuti anaopsetsa m'dziko la amoyo. 27Koma sagona pamodzi ndi amphamvu osadulidwa adagwawo amene anatsikira kumanda ndi zida zao za nkhondo, amene anawatsamiritsa malupanga ao; ndi mphulupulu zao ziri pa mafupa ao; pakuti anaopsetsa amphamvu m'dziko la amoyo. 28Ndipo udzatyoledwa pakati pa osadulidwa, nudzagona pamodzi ndi iwo ophedwa ndi lupanga. 29Edomu ali komwe, mafumu ace ndi akalonga ace onse, amene anaikidwa mu mphamvu yao, pamodzi ndi iwo ophedwa ndi lupanga; agona pamodzi ndi osadulidwa, ndi iwo akutsikira kudzenje. 30Akalonga a kumpoto ali komwe onsewo, ndi Azidoni onse, amene anatsikira pamodzi ndi ophedwa, nacita manyazi cifukwa ca kuopsetsa anacititsaku ndi mphamvu yao, nagona osadulidwa pamodzi ndi iwo ophedwa ndi lupanga, nasenza manyazi ao pamodzi ndi iwo otsikira kudzenje. 31Farao adzawaona, nadzasangalala nao aunyinji ace onse, Farao ndi ankhondo ace onse ophedwa ndi lupanga, ati Ambuye Yehova. 32Pakuti ndinaika kuopsa kwace m'dziko la amoyo; ndipo adzaikidwa pakati pa osadulidwa, pamodzi ndi iwo ophedwa ndi lupanga, ndiye Farao ndi aunyinji ace onse, ali Ambuye Yehova.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Udindo wa mneneri

1Ndipo anandidzera mau a Yehova, akuti, 2Wobadwa ndi munthu
iwe, Nena ndi ana a anthu a mtundu wako, uziti nao, Ndikafikitsira
dziko liri lonse lupanga, nakatenga eni dziko munthu wa pakati
pao, nakamuika awadikirire, 3nakaona iye lupanga lirikudzera
dziko, nakaomba lipenga ndi kucenjeza anthu; 4ndipo wina, kumva
adamva mau a lipenga, koma osalabadira, likadza lupanga,
nilimcotsa, wadziphetsa ndi mtima wace. 5Anamva mau a lipenga,
osawalabadira, wadziphetsa ndi mtima wace; akadalabadira,
akadalanditsa moyo wace. 6Koma mlonda akaona lupanga likudza,
osaomba lipenga, osacenjeza anthu, nilidza lupanga, nilicotsa mwa
iwo; munthu atengedwadi m'mphulupulu zace, koma mwazi wace
ndidzaufunsa pa dzanja la mlonda. 7Iwe tsono, wobadwa ndi
munthu, ndakuika mlonda wa nyumba ya Israyeli, m'mwemo imva
mau a pakamwa panga, nundicenjezere iwo. 8Ndikati Ine kwa
woipa, Woipawe, udzafa ndithu, osanena iwe kumcenjeza woipayo
aleke njira yace, woipa uyo adzafa m'mphulupulu yace, koma
mwazi wace ndidzaufunsa pa dzanja lako. 9Koma ukacenjeza woipa
za njira yace, aileke; koma iye osaileka njira yace, adzafa
m'mphulupulu mwace iye, koma iwe walanditsa moyo wako.
10Ndipo iwe wobadwa ndi munthu, nena kwa nyumba ya Israyeli,
Mumatero inu ndi kuti, Zolakwa zathu ndi zocimwa zathu
zitikhalira, ndipo ticita nazo liwondewonde, tidzakhala ndi moyo
bwanji? 11Uziti nao, Pali Ine, ati Ambuye Yehova, sindikondwera
nayo imfa ya woipa, koma kuti woipa aleke njira yace, nakhale ndi
moyo; bwererani, bwererani, kuleka njira zanu zoipa, muferenji inu
nyumba ya Israyeli? 12Ndipo iwe wobadwa ndi munthu, unene ndi
ana a anthu amtundu wako, Colungama ca wolungama
sicidzamlanditsa tsiku la kulakwa kwace, ndi kunena za coipa ca
woipa, sadzagwa naco tsiku lakubwerera iye kuleka coipa cace; ndi
munthu wolungama sadzakhoza kukhala ndi moyo ndi cilungamo
cace tsiku lakucimwa iye. 13Ndikanena kwa wolungama kuti
adzakhala ndi moyo ndithu, akatama cilungamo cace, akacita
cosalungama, sizikumbukika zolungama zace ziri zonse; koma
m'cosalungama cace anacicita momwemo adzafa. 14Ndipo
ndikanena kwa woipa, Udzafa ndithu: koma akabwerera iye kuleka
cimo lace, nakacita coyenera ndi colungama; 15woipayo akabweza
cikole, nakabweza ico anacilanda mwacifwamba, nakayenda
m'malemba a moyo wosacita cosalungama, adzakhala ndi moyo
ndithu, sadzafa. 16Zoipa zace ziri zonse anazicita sizidzakumbukika
zimtsutse, anacita coyenera ndi colungama; adzakhala ndi moyo
ndithu. 17Koma ana a anthu a mtundu wako akuti, Njira ya Ambuye
siiyenera; koma iwowa njira yao siiyenera. 18Akabwerera

wolungama kuleka cilungamo cace, nakacita cosalungama, adzafa m'mwemo. 19Ndipo woipa akabwerera kuleka coipa cace, nakacita coyenera ndi colungama, adzakhala ndi moyo nazo. 20Koma munati, Njira ya Ambuye siiyenera. Nyumba ya Israyeli inu, ndidzakuweruzani, yense monga mwa njira zace.

Kulangidwa kwa Aisrayeli cifukwa ca zoipa zao

21Ndipo kunali caka cakhumi ndi ciwiri ca undende wathu, mwezi wakhumi, tsiku lacisanu la mweziwo, anandidzera wina wopulumuka ku Yerusalemu, ndi kuti, Wakanthidwa mudzi. 22Koma dzanja la Yehova linandikhalira madzulo, asanandifike wopulumukayo; ndipo ananditsegula pakamwa mpaka anandifika m'mawa, m'mwemo panatseguka pakamwa panga, wosakhalanso wosalankhula. 23Ndipo anandidzera mau a Yehova, akuti, 24Wobadwa ndi munthu iwe, iwo okhala ku mabwinja a dziko la Israyeli anena, ndi kuti, Abrahamu anali yekha, nakhala nalo dziko colowa cace; koma ife ndife ambiri, dzikoli lipatsidwa kwa ife colowa cathu. 25Cifukwa cace unene nao, Atero Ambuye Yehova, Mumadyera kumodzi ndi mwazi, mumakwezera maso anu ku mafano anu, ndi kukhetsa mwazi; ndipo kodi mudzakhala nalo dziko colowa canu? 26Mumatama lupanga lanu, mumacita conyansa, mumaipsa yense mkazi wa mnansi wace; ndipo kodi mudzakhala nalo dziko colowa canu? 27Uzitero nao, Atero Ambuye Yehova, Pali Ine, iwo okhala kumabwinja adzagwadi ndi lupanga, ndi iye ali kuthengo koyera ndidzampereka kwa zirombo, adyedwe nazo; ndi iwo okhala m'malinga ndi m'mapanga adzafa ndi mliri. 28Ndipo ndidzasanduliza dziko likhale lacipululu ndi lodabwitsa, ndi mphamvu yace yodzikuza idzatha, ndi mapiri a Israyeli adzakhala acipululu, osapitako munthu. 29Pamenepo adzadziwa kuti Ine ndine Yehova, posanduliza Ine dziko likhale lacipululu ndi lodabwitsa, cifukwa ca zonyansa zao zonse anazicita. 30Ndipo iwe wobadwa ndi munthu, ana a anthu a mtundu wako anena za iwe ku makoma ndi ku makomo a nyumba zao, nanenana yense ndi mbale wace, ndi kuti, Tiyeni tikamve mau ofuma kwa Yehova. 31Ndipo akudzera monga amadzera anthu, nakhala pansi pamaso pako ngati anthu anga, namva mau ako, koma osawacita; pakuti pakamwa pao anena mwacikondi, koma mtima wao utsata phindu lao. 32Ndipo taona, akuyesa iwe ngati nyimbo yacikondi ya woyimba bwino, woyimba limba bwino; pakuti akumva mau ako, koma osawacita. 33Ndipo pakucitika ici, pakuti cifikadi, pamenepo adzadziwa kuti panali mneneri pakati pao.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Aneneratu motsutsa abusa osakhulupirika a anthu a Mulungu

1Ndipo mau a Yehova anandidzera, akuti, 2Wobadwa ndi munthu
iwe, Nenera motsutsa abusa a Israyeli; nenera, nuti nao abusawo,
Atero Ambuye Yehova, Tsoka abusa a Israyeli odzidyetsa okha; kodi
abusa sayenera kudyetsa nkhosa? 3Mukudya mafuta, mubvala
ubweya, mukupha zonenepa; koma simudyetsa nkhosa. 4Zofoka
simunazilimbitsa; yodwala simunaiciritsa, yotyoka simunailukira
chika, yopitikitsidwa simunaibweza, yotayika simunaifuna; koma
munazilamulira mwamphamvu ndi moopsa, 5M'mwemo
zinamwazika posowa mbusa, nizinakhala cakudya ca zirombo ziri
zonse za kuthengo, popeza zinamwazika. 6Nkhosa zanga
zinasokera ku mapiri ali onse, ndi pa citunda ciri conse cacitali;
inde nkhosa zanga zinabalalika pa dziko lonse lapansi, ndipo
panalibe wakuzipwaira kapena kuzifunafuna. 7Cifukwa cace abusa
inu, imvani mau a Yehova: 8Pali ine, ati Ambuye Yehova, zedi,
popeza nkhosa zanga zinakhala nyama, ndi nkhosa zanga
zinakhala cakudya ca zirombo zonse za kuthengo, cifukwa kunalibe
mbusa, ndi abusa anga sanafunafuna nkhosa zanga, koma
abusawo anadzidyetsa okha, osadyetsa nkhosa zanga; 9cifukwa
cace, abusa inu, imvani mau a Yehova: 10Atero Ambuye Yehova,
Taonani, Ine ndiipidwa nao abusa, ndidzafunsa nkhosa zanga pa
dzanja lao, ndi kuwaletsa asadyetsenso nkhosazo, ngakhale
kudzidyetsa okha sadzacitanso; ndipo ndidzalanditsa nkhosa zanga
pakamwa pao, zisakhale cakudya cao. 11Pakuti atero Ambuye
Yehova, Taonani, Ine, Inedi ndidzapwaira nkhosa zanga ndi
kuzifunafuna. 12Monga mbusa afunafuna nkhosa zace tsiku lokhala
iye pakati pa nkhosa zace zobalalika, mamwemo ndidzafunafuna
nkhosa zanga; ndipo ndidzawalanditsa m'malo monse
anabalalikamo tsiku la mitambo ndi la mdima. 13Ndipo
ndidzaziturutsa mwa mitundu ya anthu, ndi kuzisonkhanitsa
m'maiko, ndi kulowa nazo m'dziko lao; ndipo ndidzazidyetsa pa
mapiri a Israyeli, patimitsinje, ndi ponse pokhala anthu
m'dziko. 14Ndidzazidyetsa podyetsa pabwino; ndi pa mapiri atali a
Israyeli padzakhala kholo lao, apo adzagona m'khola mwabwino,
nadzadya podyetsa pokometsetsa pa mapiri a Israyeli. 15Ine
ndekha ndidzadyetsa nkhosa zanga, ndi kuzigonetsa, ati Ambuye
Yehova. 16Ndidzafuna yotayika, ndi kubweza yopitikitsidwa, ndi
kulukira chika yotyoka mwendo, ndi kulimbitsa yodwalayo; koma
yanenepa ndi yolimba ndidzazionong a, ndidzazidyetsa ndi
ciweruzo. 17Ndipo inu, gulu langa, atero Ambuye Yehova,
ndiweruza pakati pa zoweta ndi zoweta, nkhosa zamphongo ndi
atonde. 18Kodi cikuceperani, kuti mwadya podyetsa pabwino?

muyenera kodi kupondereza ndi mapazi anu podyera panu potsala? muyenera kumwa madzi ndikha, ndi kubvundulira otsalawo ndi mapazi anu? 19Ndi nkhosa zanga zidye kodi zoponderezeka ndi mapazi anu, ndi kumwa zobvunduliridwa ndi mapazi anu? 20Cifukwa cace atero nao Ambuye Yehova, Taonani, Ine, Inedi ndidzaweruza pakati pa zoweta zonenepa, ndi zoweta zoonda. 21Popeza mukankha ndi nthiti ndi phewa, nimugunda zodwala zonse ndi nyanga zanu, mpaka mwazibalalitsa kubwalo, 22cifukwa cace ndidzapulumutsa gulu langa lisakhalenso cakudya; ndipo ndidzaweruza pakati pa zoweta ndi zoweta. 23Ndipo ndidzaziutsira mbusa mmodzi; iye adzazidyetsa, ndiye mtumiki wanga Davide, iye adzazidyetsa, nadzakhala mbusa wao. 24Ndipo Ine Yehova ndidzakhala Mulungu wao, ndi mtumiki wanga Davide kalonga pakati pao; Ine Yehova ndanena. 25Ndipo ndidzapangana nazo pangano la mtendere, ndi kuleketsa zirombo zoipa m'dzikomo; ndipo zidzakhala mosatekeseka m'cipululu, ndi kugona kunkhalango. 26Pakuti ndidzaika izi ndi miraga yozungulira citunda canga; zikhale mdalitso; ndipo ndidzabvumbitsa mibvumbi m'nyengo yace, padzakhala mibvumbi ya madalitso. 27Ndi mitengo ya kuthengo idzapereka zobala zao, ndi nthaka idzapereka zipatso zace, ndipo adzakhazikika m'dziko mwao; ndipo adzadziwa kuti Ine ndine Yehova, nditadula zomangira goli lao, ndi kuwalanditsa m'manja mwa iwo akuwatumikiritsa. 28Ndipo sadzakhalanso cakudya ca amitundu, ndi cirombo ca kuthengo sicidzawadyanso; koma adzakhala osatekeseka, opanda wina wakuwaopsa. 29Ndipo ndidzawautsira mbeu yomveka, ndipo sadzacotsedwanso ndi njala m'dzikomo, kapena kusenzanso manyazi a amitundu. 30Ndipo adzadziwa kuti Ine Yehova Mulungu wao ndiri nao, ndi kuti iwo, nyumba ya Israyeli, ndiwo anthu anga, ati Ambuye Yehova. 31Ndipo inu nkhosa zanga, nkhosa za pabusa panga, ndinu anthu, ndi Ine ndine Mulungu wanu, ati Ambuye Yehova.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Aneneratu za kulangidwa kwa a ku phiri la Seiri

1Nandidzeranso mau a Yehova, akuti, 2Wobadwa ndi munthu iwe,
Lozetsa nkhope yako ku phiri la Seiri, nulinenere molitsutsa; 3nuti
nalo, Atero Ambuye Yehova, Taona, ndiipidwa nawe phiri la Seiri,
ndipo ndidzakutambasulira dzanja langa, ndi kukusanduliza
lacipululu ndi lodabwitsa. 4Ndidzapasula midzi yako, nudzakhala
lacipululu; ndipo udzadziwa kuti Ine ndine Yehova. 5Popeza uli nao
udani wosatha, waperekanso ana a Israyeli ku mphamvu ya
lupanga m'nthawi ya tsoka lao, mu nthawi ya mphulupulu
yotsiriza; 6cifukwa cace, Pali Ine, ati Ambuye Yehova,
ndikukonzeratu uphedwe, ndi mwazi udzakulondola; popeza
sunadana nao mwazi, mwazi udzakulondola. 7Ndipo ndidzaika phiri
la Seiri lodabwitsa ndi lacipululu, ndi kuononga pomwepo wopitapo
ndi wobwerapo. 8Ndipo ndidzadzaza mapiri ace ndi ophedwa ace
pa zitunda zako, ndi m'zigwa zako, ndi m'mitsinje mwako monse;
adzagwa ophedwa ndi lupanga. 9Ndidzakusandutsa mabwinja
osatha; ndi m'midzi mwako simudzakhalanso anthu; motero
mudzadziwa kuti Ine ndine Yehova, 10Popeza wanena, Mitundu iwiri
iyi ya anthu ndi maiko awiri awa adzakhala anga, tidzakhala nao
ngati colowa cathu, angakhale Yehova anali komweko; 11cifukwa
cace, Pali Ine, ati Ambuye Yehova, ndidzacita monga mwa mkwiyo
wako, ndi monga mwa nsanje yako unacita nayo pa kukwiya nao
iwe; ndipo ndidzadziwika nao pamene ndikuweruza. 12Ndipo
udzadziwa kuti Ine Yehova ndidamva zamwano zako zonse
udazinena pa mapiri a Israyeli, ndi kuti, Apasuka, apatsidwa kwa
ife tiwadye. 13Ndipo pakamwa panu mwadzikuza pa Ine, ndi
kundicurukitsira mau anu ndawamva Ine. 14Atero Ambuye Yehova,
Pokondwerera dziko lonse ndidzakusanduliza lacipululu. 15Monga
momwe unakondwerera colowa ca nyumba ya Israyeli, papeza
cidapasuka, momwemo ndidzakucitira iwe; udzakhala wopasuka,
phiri la Seiri iwe, ndi Edomu lonse lonseli; motero adzadziwa kuti
Ine ndine Yehova.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Aneneratu za mapiri a Israyeli

1Ndipo iwe, wobadwa ndi munthu, unenere kwa mapiri a Israyeli,
uziti, Mapiri a Israyeli inu, imvani mau a Yehova. 2Atero Ambuye
Yehova, Popeza mdani ananena za inu, Onyo, ingakhale misanje
yakale iri yathu, colowa cathu; 3cifukwa cace unenere, nuti, Atero
Ambuye Yehova, Cifukwa, inde cifukwa kuti anakupasulani,
nakumemezani pozungulira ponse, kuti mukhale colowa ca
amitundu otsala, ndipo mwafika pa milomo ya akazitape, ndi pa
mbiri yoipa ya anthu; 4cifukwa cace, mapiri inu a Israyeli, imvani
mau a Ambuye Yehova. Atero Ambuye Yehova kunena ndi mapiri,
ndi zitunda, ndi mitsinje, ndi zigwa, ndi zipululu zopasuka, ndi
midzi yamabwinja, imene yakhala cakudya ndi coseketsa amitundu
otsala akuzungulira; 5cifukwa cace atero Ambuye Yehova, Zoonadi
pa nsanje yanga yodya nayo moto ndinanena motsutsana nao
amitundu otsala, ndi Edomu lonse, amene anadzipatsira dziko
langa likhale colowa cao ndi cimwemwe ca mtima wonse, ndi,
mtima wopeputsa, kuti alande zace zonse zikhale
zofunkha. 6Cifukwa cace unenere za dziko la Israyeli, nuti kwa
mapiri ndi kwa zitunda, kwa mitsinje ndi kwa zigwa, Atero Ambuye
Yehova, Taonani, ndalankhula mu nsanje yanga ndi ukali wanga,
popeza mwasenza manyazi a amitundu; 7cifukwa cace atero
Ambuye Yehova, Ndakweza dzanja langa Ine, ndi kuti, Zedi
amitundu akuzungulira inu adzasenza manyazi ao. 8Koma inu,
mapiri a Israyeli, mudzaphukitsa nthambi zanu, ndi kubalira anthu
anga Israyeli zipatso zanu, pakuti ayandikira kufika. 9Pakuti
taonani, Ine ndikhalira nanu kumodzi, ndipo
ndidzakutembenukirani; ndipo mudzabzalidwa ndi
kupaliridwa, 10ndipo ndidzakucurukitsirani anthu nyumba yonse ya
Israyeli, yonseyi, ndi m'midzimo mudzakhala anthu, ndi
kumabwinja kudzamangidwa midzi. 11Ndipo ndidzakucurukitsirani
anthu ndi nyama; ndipo adzacuruka, nadzabalana; ndipo
ndidzakhalitsa anthu pa inu, monga umo anakhalira kale, ndipo
ndidzacitira inu zabwino koposa poyamba paja; motero
mudzadziwa kuti Ine ndine Yehova. 12Ndipo ndidzayendetsa anthu
pa inu, ndiwo anthu anga Israyeli; adzakhala nawe dziko lao lao,
ndipo udzakhala colowa cao osafetsanso ana ao. 13Atero Ambuye
Yehova, Popeza akuti nawe, Dzikowe ukudya anthu, nuyesa anthu
ako afedwa; 14cifukwa cace sudzadyanso anthu, kapena kuyesanso
amtundu wako afedwa, ati Ambuye Yehova. 15Ndipo
sindidzakumvetsanso za manyazi a amitundu, ndipo
sudzaseozanso mtonzo wa mitundu ya anthu, kapena
kukhumudwitsanso anthu ako, ati Ambuye Yehova.

Za kukonzekanso kwa Israyeli

16Mau a Yehova anandidzeranso, ndi kuti, 17Wobadwa ndi munthu iwe, muja a nyumba ya Israyeli anakhala m'dziko mwao, analidetsa ndi njira yao, ndi macitidwe ao; njira yao pamaso panga inanga cidetso ca mkazi wooloka. 18M'mwemo ndinawatsanulira ukali wanga, cifukwa ca mwazi anautsanulira padziko, ndi cifukwa ca mafano analidetsa dziko nao; 19ndipo ndinawabalalitsa mwa amitundu, namwazika m'maiko monga mwa njira yao; ndi monga mwa macitidwe ao ndinawaweruza. 20Ndipo pofika iwo kwa amitundu kumene anamukako, anadetsa dzina langa loyera; popeza anthu ananena za iwowa, Awa ndi anthu a Yehova, naturuka m'dziko mwace. 21Koma ndinawaleka cifukwa ca dzina langa loyera, limene a nyumba ya Israyeli adalidetsa pakati pa amitundu, kumene adarakako, 22Cifukwa cace nena kwa nyumba ya Israyeli, Atero Ambuye Yehova, Sindicicita ici cifukwa ca inu, nyumba ya Israyeli, koma cifukwa ca dzina langa loyera munaliipsalo pakati pa amitundu, kumene mudamukako. 23Ndipo ndidzazindikiritsa dzina langa lalikuru kuti liri loyera, limene laipitsidwa mwa amitundu, limene inu munaliipsa pakati pao; ndipo amitundu adzadziwa kuti Ine ndine Yehova, ati Ambuye Yehova, pozindikiridwa Ine woyera mwa inu pamaso pao. 24Pakuti ndidzakutengani kukuturutsani kwa amitundu, ndi kukusokolotsani m'maiko onse, ndi kubwera nanu m'dziko lanu. 25Ndipo ndidzakuwazani madzi oyera, ndipo mudzakhala oyera; ndidzakuyeretsani kukucotserani zodetsa zanu zonse, ndi mafano anu onse. 26Ndipo ndidzakupatsani mtima watsopano, ndi kulonga m'kati mwanu mzimu watsopano; ndipo ndidzacotsa mtima wamwala m'thupi, ndi kukupatsani mtima wamnofu. 27Ndipo ndidzaika mzimu wanga m'kati mwanu, ndi kukuyendetsani m'malemba anga; ndipo mudzasunga maweruzo anga ndi kuwacita. 28Ndipo mudzakhala m'dziko ndinapatsa makolo anulo, ndipo mudzakhala anthu anga, ndi Ine ndidzakhala Mulungu wanu. 29Ndipo ndidzakupulumutsani kwa zodetsa zanu zonse, ndidzaitananso tirigu ndi kumcurukitsa, osaikiranso inu njala. 30Ndipo ndidzacurukitsa zobala za mitengo, ndi zipatso za m'munda, kuti musalandirenso citonzo ca njala mwa amitundu. 31Pamenepo mudzakumbukila njira zanu zoipa, ndi zocita inu zimene sizinali zabwino; ndipo mudzanyansidwa nokha pamaso panu, cifukwa ca mphulupulu zanu ndi zonyansa zanu. 32Dziwani kuti sindicita ici cifukwa ca inu, ati Ambuye Yehova; citani manyazi, dodomani, cifukwa ca njira zanu, nyumba ya Israyeli inu. 33Atero Ambuye Yehova, Tsiku loti ndikuyeretsani kukucotserani mphulupulu zanu zonse, ndidzakhalitsa anthu m'midzimo; ndi pamabwinja padzamangidwa. 34Ndi dziko lacipululu lidzalimidwa, cinkana linali lacipululu pamaso pa onse

opitako. 35Ndipo adzati, Dziko ili lacipululu lasanduka ngati munda
wa Edene, ndi midzi yamabwinja, ndi yacipululu, ndi yopasuka,
yamangidwa malinga, muli anthu m'mwemo. 36Pamenepo
amitundu otsala pozungulira panu adzadziwa kuti Ine Yehova
ndamanga malo opasuka, ndi kubzala pamene panali cipululu; Ine
Yehova ndanena ndidzacita.
37Atero Ambuye Yehova, Ici comwe adzandipempha a nyumba ya
Israyeli ndiwacitire ici, ndidzawacurukitsira anthu ngati
nkhosa. 38Ngati nkhosa za nsembe, ngati nkhosa za ku Yerusalemu
pa madyerero ace oikika, momwemo midzi yamabwinja idzadzala
nao magulu a anthu; motero adzadziwa kuti Ine ndine Yehova.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masomphenya a mafupa

1Dzanja la Yehova linandikhalira, ndipo anaturuka nane mu mzimu
wa Yehova, nandiika m'kati mwa cigwa, ndico codzala ndi
mafupa; 2ndipo anandipititsa pamenepo pozungulira ponse, ndipo
taonani, anali aunyinji pacigwa pansi, ndipo anaumitsitsa. 3Ndipo
anati kwa ine, Wobadwa ndi munthu iwe, mafupa awa nkukhala ndi
moyo kodi? Ndipo ndinati, Ambuye Yehova, mudziwa
ndinu. 4Pamenepo anati kwa ine, Nenera kwa mafupa awa, nuti
nao, Mafupa ouma inu, imvani mau a Yehova. 5Atero Ambuye
Yehova kwa mafupa awa, Taonani, ndidzalonga mpweya mwa inu,
ndipo mudzakhala ndi moyo. 6Ndipo ndidzakuikirani mtsempha,
ndi kufikitsira inu mnofu, ndi kukuta inu ndi khungu, ndi kulonga
mpweya mwa inu; ndipo mudzakhala ndi moyo; motero
mudzadziwa kuti Ine ndine Yehoya. 7M'mwemo ndinanenera
monga anandiuza, ndipo ponenera ine panali phokoso; ndipo
taonani, panali gobede gobede, ndi mafupa anasendererana,
pfupa kutsata pfupa linzace. 8Ndipo ndinapenya, taonani, panali
mitsempha pa iwo, panadzaponso mnofu, ndi khungu linawakuta
pamwamba pace; koma munalibe mpweya mwa iwo. 9Ndipo anati
kwa ine, Nenera kwa mpweya, nenera, wobadwa ndi munthu iwe,
nuti kwa mpweya, Atero Ambuye Yehova, Idza, mpweya iwe,
kucokera ku mphepo zinai, nuuzire ophedwa awa, kuti akhale ndi
moyo. 10M'mwemo ndinanenera monga anandiuza, ndi mpweya
unawalowa, ndipo anakhala ndi moyo, naimirira ciriri, gulu la
nkhondo lalikurukuru ndithu. 11Pamenepo anati kwa ine, Wobadwa
ndi munthu iwe, Mafupa awa ndiwo nyumba yonse ya Israyeli;
taonani, akuti, Mafupa athu auma, ciyembekezo cathu catayika,
talikhidwa. 12Cifukwa cace, nenera, nunene nao, Atero Ambuye
Yehova, Taonani anthu anga, ndidzatsegula kumanda kwanu, ndi
kukweza inu muturuke m'manda mwanu, ndipo ndidzakulowetsani
m'dziko la Israyeli. 13Ndipo mudzadziwa kuti Ine ndine. Yehova
potsegula Ine kumanda kwanu, ndi kukweza inu kukuturutsani
m'manda mwanu, anthu anga inu. 14Ndipo ndidzalonga mzimu
wanga mwa inu, nimudzakhala ndi moyo; ndipo ndidzakukhazikani
m'dziko mwanu; motero mudzadziwa kuti Ine Yehova ndanena ndi
kucicita, ati Yehova.
15Anandidzeranso mau a Yehova, akuti, 16Tsono, iwe wobadwa ndi
munthu, Tenga mtengo umodzi, nulembepo, Wa Yuda ndi wa ana a
Israyeli anzace; nutenge mtengo wina, nulembepo, Wa Yosefe,
mtengo wa Efraimu, ndi wa nyumba yonse ya Israyeli
anzace; 17nuiphatikize wina ndi unzace ikhale mtengo umodzi
m'dzanja lako. 18Ndipo ana a anthu amtundu wako akanena ndi
iwe, ndi kuti, Sutifotokozera nanga zitani izi? 19unene nao, Atero

Ambuye Yehova, Taonani, ndidzatenga mtengo wa Yosefe uli
m'dzanja la Efraimu, ndi wa mafuko a Israyeli anzace, ndi kuwaika
pamodzi ndi mtengo wa Yuda, ndi kuiyesa mtengo umodzi; ndipo
idzakhala umodzi m'dzanja langa. 20Ndipo mitengo imene
ulembapo idzakhala m'dzanja mwako pamaso pao. 21Nunene nao,
Atero Ambuye Yehova, Taonani, ndidzatenga ana a Israyeli pakati
pa amitundu kumene adamkako, ndi kuwasokolotsa ku mbali
zonse, ndi kulowa nao m'dziko mwao; 22ndipo ndidzawayesa
mtundu umodzi m'dzikomo, pa mapiri a Israyeli; ndipo mfumu
imodzi idzakhala mfumu ya iwo onse, sadzakhalanso mitundu iwiri,
kapena kugawanikanso maufumu awiri konse ai. 23Ndipo
sadzadzidetsanso ndi mafano ao, kapena ndi zonyansa zao,
kapena ndi zolakwa zao ziri zonse; koma ndidzawapulumutsa
mokhala mwao monse m'mene anacimwamo, ndi kuwayeretsa;
m'mwemo adzakhala anthu anga, ndi Ine ndidzakhala Mulungu
wao. 24Ndi mtumiki wanga Davide adzakhala mfumu yao, ndipo
iwo onse adzakhala ndi mbusa mmodzi, adzayendanso
m'maweruzo anga, nadzasunga malemba anga ndi
kuwacita. 25Ndipo adzakhala m'dziko ndinalipereka kwa Yakobo
mtumiki wanga, limene anakhalamo makolo anu, ndipo adzakhala
m'mwemo iwo, ndi ana ao, ndi zidzukulu zao kosatha; ndi Davide
mtumiki wanga adzakhala mtsogoleri wao kosatha. 26Ndipo
ndidzapangana nao pangano la mtendere, lidzakhala pangano
losatha nao, ndipo ndidzawakhazika, ndi kuwacurukitsa, ndi kuika
malo anga opatulika pakati pao kosatha. 27Kacisi wanganso
adzakhala nao, ndipo Ine ndidzakhala Mulungu wao, ndi iwo
adzakhala anthu anga. 28Ndipo amitundu adzadziwa kuti Ine ndine
Yehova wakupatula Israyeli, pokhala pakati pao malo anga
opatulika kosatha.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Anereratu za kulangidwa kwa Gogi

1Ndipo anandidzera mau a Yehova, akuti, 2Wobadwa ndi munthu
iwe, lozetsa nkhope yako kwa Gogi, wa ku dziko la Magogi, ndiye
mfumu yaikuru ya Meseki ndi Tubala; 3nunenere motsutsana naye,
uziti, Atero Ambuye Yehova, Taona, nditsutsana nawe, Gogi iwe,
mfumu yaikuru ya Meseki ndi Tubala; 4ndipo ndidzakutembenuza
ndi kukowa m'cibwano mwako ndi zokowera, ndi kukuturutsa ndi
nkhondo yako yonse, akavalo ndi apakavalo obvala mokwanira
onsewo, msonkhano waukuru ndi zikopa zocinjiriza, onsewo
ogwira, bwino malupanga; 5Perisiya, Kusi, ndi Puti pamodzi nao,
onsewo ndi cikopa ndi cisoti cacitsulo; 6Gomeri ndi magulu ace
onse, nyumba ya Togarima, ku malekezero a kumpoto, ndi magulu
ace onse, mitundu yambiri pamodzi ndi iwe. 7Ukonzekeretu, Inde
udzikonzeretu, iwe ndi msonkhano wako wonse unakusonkhanira,
nukhale iwe mtsogoleri wao. 8Atapita masiku ambiri
udzakumbukirika; zaka zotsiriza udzalowa m'dziko lobwezedwa
lopulumuka lupanga, losonkhanidwa lituruke m'mitundu yambiri ya
anthu, pa mapiri a Israyeli, amene adakhala acipululu cikhalire;
koma liturutsidwa m'mitundu ya anthu, ndipo adzakhala
mosatekeseka onsewo. 9Ndipo udzakwera udzadza ngati mkuntho,
udzanga mtambo kuphimba dziko, iwe ndi magulu ako onse, ndi
mitundu yambiri ya anthu pamodzi ndi iwe. 10Atero Ambuye
Yehova, Kudzacitika tsiku ilo kuti m'mtima mwako mudzalowa
zinthu, nudzalingirira ciwembu coipa, 11nudzati, Ndidzakwera
kumka ku dziko la midzi yopanda malinga, ndidzamka kwa iwo
amtendere okhala mosatekeseka, onsewo akukhala opanda
malinga, opanda mipingiridzo, kapena zitseko; 12kulanda ndi
kufunkha zao, kubweza dzanja lako liononge mopasuka muli anthu
tsopano, liononge mtundu wa anthu osonkhanidwa mwa amitundu,
odzionera zoweta ndi cuma, okhala pakati pa dziko. 13Seba, ndi
Dedani, ndi amalonda a Tarisi, ndi misona yace yonse ya mikango
adzati kwa iwe, Wadza kodi kudzafunkha? wasonkhanitsa kodi
msonkhano wako kulanda, kucoka nazo siliva ndi golidi, kucoka
nazo zoweta ndi cuma, kulanda zankhondo zambiri?
14Cifukwa cace nenera, wobadwa ndi munthu iwe, uziti kwa Gogi,
Atero Ambuye Yehova, Tsiku ilo, pokhala mosatekeseka anthu anga
Israyeli, sudzacidziwa kodi? 15Ndipo udzaturuka m'malo mwako
m'malekezero a kumpoto, iwe ndi mitundu yambiri ya anthu
pamodzi ndi iwe, onsewo apakavalo, msonkhano waukuru ndi
nkhondo yaikuru; 16ndipo udzakwerera anthu anga Israyeli ngati
mtambo wakuphimba dziko; kudzacitika masiku otsiriza
ndidzabwera nawe ulimbane nalo dziko langa, kuti amitundu
andidziwe, pozindikiridwa Ine woyera mwa iwe, Gogi, pamaso

pao. 17Atero Ambuye Yehova, Kodi iwe ndiwe iye amene ndinanena
za iye masiku akale mwa atumiki anga aneneri a Israyeli,
akunenera masiku aja za zaka za m'tsogolo, kuti ndidzabwera
nawe kulimbana nao? 18Ndipo kudzacitika tsiku ilo, tsiku loti Gogi
adzadza kulimbana ndi dziko la Israyeli, ati Ambuye Yehova, ukali
wanga udzakwera m'mphuno mwanga. 19Pakuti ndanena mu
nsanje yanga, ndi m'moto wa kuzaza kwanga, Zoonadi tsiku ilo
kudzakhala kugwedezeka kwakukuru m'dziko la Israyeli; 20motero
kuti nsomba za m'nyanja, ndi mbalame za m'mlengalenga, ndi
nyama za kuthengo, ndi zokwawa zonse zakukwawa pansi, ndi
anthu onse akukhala padziko, zidzanjenjemera pamaso panga; ndi
mapiri adzagwetsedwa, ndi potsetsereka padzagumuka, ndi
makoma onse adzagwa pansi. 21Ndipo ndidzamuitanira lupanga ku
mapiri anga onse, ati Ambuye Yehova, munthu ali yense lupanga
lace lidzaombana nalo la mbale wace. 22Ndipo ndidzalimbana naye
ndi mliri ndi mwazi; ndipo ndidzambvumbitsira iye, ndi magulu
ace, ndi mitundu yambiri ya anthu okhala naye mbvumbi waukuru,
ndi matalala akuru, moto ndi sulfure. 23Momwemo
ndidzadzikuzitsa, ndi kudzizindikiritsa woyera, ndipo ndidzadziwika
pamaso pa amitundu ambiri; motero adzadziwa kuti Ine ndine
Yehova.

©The Bible Society of Malawi, 1992

1Ndipo iwe, wobadwa ndi munthu, nenera motsutsana naye Gogi,
uziti, Atero Ambuye Yehova, Taona, nditsutsana nawe Gogi, iwe
mfumu yaikuru ya Meseki ndi Tubala; 2ndipo ndidzakutembenuza,
ndi kukutsogolera, ndi kukweza iwe ucoke ku malekezero a
kumpoto; ndipo ndidzadza nawe ku mapiri a Israyeli; 3ndipo
ndidzakantha uta wako kuucotsa m'dzanja lako lamanzere, ndi
kutayitsa mibvi yako ku dzanja lako lamanja. 4Udzagwa pa mapiri a
Israyeli, iwe ndi magulu ako onse, ndi mitundu ya anthu okhala ndi
iwe; ndidzakupereka kwa mbalame zolusa za mitundu yonse, ndi
kwa zirombo za kuthengo, akuyese cakudya. 5Udzagwa kuthengo
koyera, pakuti ndanena ndine, ati Ambuye Yehova. 6Ndipo
ndidzatumizira moto Magogi, ndi iwo okhala mosatekeseka
m'zisumbu; motero adzadziwa kuti Ine ndine Yehova. 7Ndipo
ndidzadziwikitsa dzina langa loyera pakati pa anthu anga Israyeli,
osalola dzina langa loyera aliipsenso; ndipo amitundu adzadziwa
kuti Ine ndine Yehova Woyerayo wa Israyeli. 8Taonani, cikudza,
cidzacitika, ati Ambuye Yehova, ndilo tsiku ndanenalo. 9Ndipo iwo
okhala m'midzi ya Israyeli adzaturuka, nadzasonkha moto,
nadzatentha zida za nkhondo, ndi zikopa zocinjiriza, mauta, ndi
mibvi, ndi ndodo, ndi mikondo; ndipo adzasonkha moto nazo zaka
zisanu ndi ziwiri; 10osatenga nkhuni kuthengo, kapena kuzitema
kunkhalango; popeza adzasonkha moto ndi zidazo; nadzafunkha
iwo amene anawafunkha, ndi kulanda zao za iwo adalanda zaozo,
ati Ambuye Yehova.
11Ndipo kudzacitika tsiku ilo, ndidzapatsa Gogi manda m'Israyeli,
cigwa ca opitawo kum'mawa kwa nyanja; ndipo lidzaletsa opitawo,
ndipo adzaika komweko Gogi ndi unyinji wace wonse, nadzacicha,
Cigwa ca unyinji wa Gogi. 12Ndi a nyumba ya Israyeli adzapititsa
miyezi isanu ndi iwiri alikuwaika, kuti ayeretse dziko. 13Inde anthu
onse a m'dziko adzawaika, nadzamveka nako tsiku
lakulemekezedwa Ine, ati Ambuye Yehova. 14Ndipo adzasankha
anthu akupita-pitabe m'dziko, ndi pamodzi ndi opitapitawo anthu
akuika mafupa otsala pamtunda, kuliyeretsa; pakutha miyezi isanu
ndi iwiri adzapwaira. 15Ndipo opitapitawo adzapitapita m'dziko,
ndipo winaakaona pfupa la munthu aikepo cizindikilo, mpaka
oikawo aliika m'cigwa ca unyinji wa Gogi. 16Ndipo dzina la mudzi
lidzakhala Hamona. Momwemo adzayeretsa dziko.
17Ndipo iwe, wobadwa ndi munthu, atero Ambuye Yehova, Nena
kwa mbalame za mitundu yonse, ndi kwa nyama zonse za
kuthengo, Memezanani, idzani, sonkhanani ku mbali zonse, kudza
ku nsembe yanga imene ndikupherani, ndiyo nsembe yaikuru pa
mapiri a Israyeli, kuti mudzadye nyama ndi kumwa
mwazi. 18Mudzadya nyama ya amphamvu, ndi kumwa mwazi wa

akalonga a padziko, wa nkhosa zamphongo, wa ana a nkhosa, ndi wa mbuzi, ndi wa ng'ombe, zonsezi zonenepa za ku Basana. 19Ndipo mudzadya zonona mpaka mudzakhuta, ndi kumwa mwazi mpaka mudzaledzera za nsembe yanga ndakupherani. 20Ndipo podyera panga mudzakhuta akavalo, ndi magareta, ndi anthu amphamvu, ndi anthu onse a nkhondo, ati Ambuye Yehova. 21Ndipo ndidzaika ulemerero wanga mwa amitundu; ndi amitundu onse adzaona ciweruzo canga ndacicita, ndi dzanja langa limene ndinawaikira. 22Ndipo nyumba ya Israyeli idzadziwa kuti Ine ndine Yehova Mulungu wao, kuyambira tsiku ilo ndi m'tsogolomo. 23Ndipo amitundu adzadziwa kuti nyumba ya Israyeli idalowa undende cifukwa ca mphulupulu zao, popeza anandilakwira Ine; ndipo ndinawabisira nkhope yanga; m'mwemo ndinawapereka m'dzanja la adani ao, nagwa iwo onse ndi lupanga. 24Ndinacita nao monga mwa kudetsedwa kwao, ndi monga mwa kulakwa kwao, ndipo ndinawabisira nkhope yanga. 25Cifukwa cace atero Ambuye Yehova, Tsopano ndidzabweza undende wa Yakobo, ndi kucitira cifundo nyumba yonse ya Israyeli, ndipo ndidzacitira dzina langa loyera nsanje. 26Ndipo adzasenza manyazi ao, ndi zolakwa zao zonse, zimene anandilakwira nazo, pokhala mosatekeseka iwo m'dziko lao, opanda wina wakuwaopsa; 27nditabwera nao kucoka kwa mitundu ya anthu, nditawasokolotsa m'maiko a adani ao, ndi kuzindikiridwa Woyera mwa iwo pamaso pa amitundu ambiri. 28Ndipo adzadziwa kuti Ine ndine Yehova Mulungu wao, popeza ndinalola atengedwe ndende kumka kwa amitundu, koma ndinawasonkhanitsanso akhale m'dziko lao, osasiyakonso mmodzi yense wa iwowa. 29Ndipo sindidzawabisiranso nkhope yanga, popeza ndatsanulira mzimu wanga pa nyumba ya Israyeli, ati Ambuye Yehova.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masomphenya a Ezekieli, kukonzekanso kwa Kacisi ndi mabwalo ace

1Caka ca makumi awiri ndi zisanu ca undende wathu, poyamba caka, tsiku lakhumi lamwezi, caka cakhumi ndi zinai atakantha mudziwo, tsiku lomwelo, dzanja la Mulungu linandikhalira; ndipo anamuka nane komweko. 2M'masomphenya a Mulungu Iye anabwera nane m'dziko la Israyeli, nandikhalitsa pa phiri lalitali ndithu; pamenepo panali ngati mamangidwe a mudzi kumwela, 3Ndipo anamuka nane komweko, ndipo taona, panali munthu, maonekedwe ace ngati amkuwa, ndi cingwe cabwazi m'dzanja lace, ndi bango loyesa nalo, naima kucipata iye. 4Ndipo munthuyu anati kwa ine, Wobadwa ndi munthu iwe, penya ndi maso ako, imva m'makutu mwako, nuike mtima wako pa zonse ndidzakuonetsa iwe; pakuti unatengedwa kudza kuno, kuti ndikuonetse izi; fotokozera nyumba ya Israyeli zonse uziona. 5Ndipo taonani, panali linga kunja kwace kwa nyumba ya kacisi poizinga, ndi m'dzanja lace la munthuyo bango loyesa nalo la mikono isanu ndi umodzi, mkono uli wonse mkono kudza cikhato; ndipo anayesa cimangidweco kucindikira kwace bango limodzi, ndi msinkhu wace bango limodzi. 6Pamenepo anafika ku cipata coloza kum'mawa, nakwera pa makwerero ace; ndipo anayesa ciundo ca cipata, bango limodzi kucindikira kwace; ndico ciundo coyamba, bango limodzi. 7Ndi cipinda ca alonda, conse nca bango limodzi m'litali mwace, ndi bango limodzi kupingasa kwace, ndi pakati pa zipinda za alonda mikono isanu, ndi ciundo ca cipata ku mbali ya ku khonde la kucipata m'katimo, bango limodzi. 8Anayesanso khonde la kucipata ku mbali ya kukacisi, bango limodzi. 9Pamenepo anayesa khonde la kucipata mikono isanu ndi itatu, ndi mphuthu zace mikono iwiri; ndi khonde la kucipata linaloza kukacisi. 10Ndi zipinda za alonda za ku cipata ca kum'mawa ndizo zitatu cakuno, ndi zitatu cauko, zitatuzi nza muyeso umodzimodzi, ndi mphuthuzo nza muyeso umodzimodzi, cakuno ndi cauko. 11Ndipo anayesa kupingasa kwa cipata pakhoma pace mikono khumi, ndi utali wace wa cipata mikono khumi ndi itatu; 12ndi pakhomo pa zipinda za alonda panali kakhoma ka mkono umodzi cakuno, ndi kakhoma ka mkono umodzi cauko; ndi zipinda za alonda mikono isanu ndi umodzi cakuno, ndi mikono isanu ndi umodzi cauko. 13Ndipo anayesa cipata kuyambira ku tsindwi la cipinda ca alonda cimodzi, kufikira ku tsindwi la cinzace, kupingasa kwace ndiko mikono makumi awiri ndi isanu; makomo napenyana. 14Anamanganso nsaaamira za mikono makumi asanu ndi limodzi; ndi bwalo la pakati pa cipata lidafikira kunsanamira. 15Ndipo kuyambira pa khomo lolowera la cipata

kufikira khomo la khonde la cipata m'katimo ndiko mikono makumi asanu. 16Ndipo panali mazenera a made okhazikika pazipinda ndi m'makhoma a pakati pao, m'kati mwa cipata pozungulira ponse; momwemonso pazidundumwa; ndipo panali mazenera pozungulira ponse m'katimo, pa nsanamirazo panali akanjedza.
17Pamenepo analowa nane ku bwalo lakunja, ndipo taonani, panali zipinda, ndi moyalidwa miyala mokonzekera bwalo pozungulira ponse; moyalidwa miyalamo munali zipinda makumi atatu. 18Ndipo moyalidwamo munali pa mbali ya zipata molingana ndi utali wace wa zipata, ndimo moyalidwa mwamunsi. 19Pamenepo anayesa kupingasa kwace kuyambira pakhomo pace pacipata cakunsi, kufikira kumaso kwace kwa bwalo la m'kati kunja kwace, mikono zana kum'mawa, ndi kumpoto. 20Ndi cipata ca bwalo lakunja coloza kumpoto anaciyesa m'litali mwace, ndi kupingasa kwace. 21Ndi zipinda zace ndizo zitatu cakuno, ndi zitatu cauko, ndi makhoma a pakati pace; ndi zidundumwa zace zinali monga mwa muyeso wa cipata coyambaco, m'litali mwace mikono makumi asanu, ndi kupingasa kwace mikono makumi awiri mphambu isanu. 22Ndi mazenera ace, ndi zidundumwa zace, ndi akanjedza ace, anali monga mwa muyeso wa cipata coloza kum'mawa; ndipo anakwerako ndi makwerero asanu ndi awiri, ndi zidundumwa zace zinali pakhomo. 23Ndipo panali cipata ca bwalo lam'kati, copenyana ndi cipata cinzace cakunja kumpoto, ndi ca kum'mawa; ndipo anayesa kuyambira kucipata kufikira kucipata mikono zana. 24Ndipo ananditsogolera kumka kumwela, ndipo taonani, panali cipata kumwela, nayesa makhoma a pakati pace, ndi zidundumwa zace, monga mwa miyeso yomweyi. 25Ndimo munali mazenera m'menemo, ndi m'zidundumwa zace pozungulirapo, monga mazenera ena aja, m'litali mwace mikono makumi asanu, ndi kupingasa kwace mikono makumi awiri mphambu isanu. 26Ndipo panali makwerero asanu ndi awiri okwererapo, ndi zidundumwa zace kumaso kwace; ndi pa nsanamira zace cakuno ndi cauko panali akanjedza. 27Ndipo panali cipata ca bwalo lam'kati cakulozakumwela, nayesa kuyambira kucipata kufikira kucipata kumwela mikono zana.
28Pamenepo analowa nane pa cipata ca kumwela m'bwalo lam'kati, nayesa cipata ca kumwera, monga mwa miyeso yomweyi; 29ndi zipinda zace, ndi makhoma a pakati pace, ndi zidundumwa zace, monga mwa miyeso yomweyi; ndimo munali mazenera m'menemo, ndi m'zidundumwa zace pozungulirapo; m'litali mwace mikono makumi asanu, ndi kupingasa kwace mikono makumi awiri mphambu isanu. 30Ndipo panali zidundumwa pozungulirapo, m'litali mwace mikono makumi awiri mphambu isanu, ndi kupingasa kwace mikono isanu. 31Ndi zidundumwa zace

zinaloza ku bwalo lakunja, ndi pa nsanamira zace panali akanjedza, ndi pokwererapo panali makwerero asanu ndi atatu. 32Ndipo analowa ndine m'bwalo lam'kati kuloza kum'mawa, nayesa cipata ca kum'mawa monga mwa miyeso yomweyi; 33ndi zipindazace, ndi makhoma a pakati pace, Indi zikundumwa zace, monga mwa miyeso yomweyi; ndimo munali mazenera m'menemo, ndi m'zidundumwa zace pozungulirapo, m'litali mwace mikono makumi asanu, ndi kupingasa kwace mikono makumi awiri mphambu isanu. 34Ndi zidundumwa zace zinaloza ku bwalo lakunja; ndi pa nsanamira zace panali akanjedza cakuno ndi cauko; ndipo pokwerera pace panali makwerero asanu ndi atatu. 35Pamenepo anabwera nane ku cipata ca kumpoto, naciyesa monga mwa miyeso yomweyi; 36zipinda zace, makhoma a pakati pace, ndi zidundumwa zace; ndimo munali mazenera m'menemo pozungulirapo, m'litali mwace mikono makumi asanu, ndi kupingasa kwace mikono makumi awiri mphambu isanu. 37Ndi nsanamira zace zinaloza ku bwalo lakunja; ndi pa nsanamira zace panali akanjedza cakuno ndi cauko; ndipo pokwerera pace panali makwerero asanu ndi atatu.
38Ndipo pa nsanamira za pazipata panali kanyumba ndi citseko cace; pamenepo anatsuka nsembe vopsereza. 39Ndipo m'khonde la pacipata munali magome awiri cakuno, ndi magome awiri cauko, kuti apherepo nsembe yopsereza, ndi nsembe yaucimo, ndi nsembe yoparamula. 40Ndi ku mbali yina ya khonde kunja, pakukwerera polowera pa cipata ca kumpoto, kunali magome awiri, ndi ku mbali inzace ya kucipata kunali magome awiri. 41Magome anai cakuno, ndi magome anai cauko, ku mbali ya cipata; magome asanu ndi atatu, amene anapherapo nsembe. 42Ndipo panali magome anai a nsembe yopsereza a miyala yosema, m'litali mwace mkono ndi nusu, kupingasa kwace mkono ndi nusu, msinkhu wace mkono umodzi; pamenepo adafoika zipangizo zimene anaphera nazo nsembe yopsereza ndi nsembe yophera. 43Ndi ziciri zangowe, cikhato m'litali mwace, zinamangika m'katimo pozungulirapo; ndi pamagome panali nyama ya nsembe. 44Ndi kunja kwa cipata ca m'kati kunali tinyumba ta oyimba m'bwalo lam'kati, ku mbali ya cipata ca kumpoto; ndipo tinaloza kumwela, kena ku mbali ya cipata ca kum'mawa kanaloza kumpoto. 45Ndipo anati kwa ine, Kanyumba aka koloza kumwela nka ansembe odikira kacisi. 46Ndi kanyumba koloza kumpoto nka ansembe odikira guwa la nsembe, ndiwo ana a Zadoki amene ayandikira kwa Yehova mwa ana a Levi, kumtumikira Iye. 47Ndipo anayesa bwalolo mikono zana m'litali mwace, ndi mikono zana kupingasa kwace, lamphwamphwa; ndi guwa la nsembe linali kukhomo kwa nyumba.

48Pamenepo anadza nane ku khonde la kacisi, nayesa mphuthu za
khonde, mikono isanu cakuno, ndi mikono isanu cauko; ndi
kupingasa kwa cipata, mikono itatu cakuno, ndi mikono itatu
cauko. 49M'litali mwace mwa khonde mikono makumi awiri, ndi
kupingasa kwace mikono khumi ndi umodzi; ndipo panali
makwerero khumi okwerera kumeneko; ndipo panali zoimiritsa pa
nsanamirazo, imodzi cakuno, ndi imodzi cauko.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Kukonzekanso kwa Kacisi: malo opatulikitsa

1Ndipo anadza nane ku Kacisi, nayesa nsanamira zace, kupingasa
kwace mikono isanu ndi umodzi cakuno, ndi mikono isanu ndi
umodzi cauko, ndiko kupingasa kwa cihema cija. 2Ndi kupingasa
kwa khomo mikono khumi; ndi mbali za khomo mikono isanu
cakuno, ndi mikono isanu cauko; nayesa malo opatulika, m'litali
mwace mikono makumi anai, ndi kupingasa kwace mikono makumi
awiri. 3Nalowa m'katimo, nayesa mphuthu za pakhomo mikono
iwiri, ndi msinkhu wa khomo mikono isanu ndi umodzi, ndi
kupingasa kwa khomo mikono isanu ndi iwiri. 4Anayesanso m'kati
mwa Kacisi m'tsogolomo, m'litali mwace mikono makumi awiri, ndi
kupingasa kwace mikono makumi awiri; ndipo anati kwa ine, Umo
m'mopatulikitsa. 5Pamenepo anayesa khoma la nyumba,
kucindikira kwace mikono isanu ndi umodzi, ndi kupingasa kwace
kwa zipinda za m'mphepete mikono inai, pozungulira pace ponse
pa kacisi. 6Ndipo zipinda za m'mphepete zinasanjikizana cina pa
cinzace; zinatero makumi atatu mizere yonse itatu, nizinalowa ku
khoma locirikiza zipinda za m'mphepete pozungulirapo, zisanjikike
pamenepo; pakuti sizinagwiridwa ndi khoma la nyumba. 7Ndipo
zipinda za m'mphepete zinakula m'kupingasa kwao, pozinga
nyumba m'kukwera kwao; pakuti nyumba inazingika
mokwerakwera pozungulira pace pa nyumba; motero kupingasa
kwace kwa nyumba kunakula kumwamba kwace, momwemonso
anakwera kuyambira cipinda cakunsi, kupita capakati, kufikira
cam'mwamba. 8Ndinaonanso kuti kunyumba kunali ciunda
pozungulira pace; maziko a zipinda za m'mphepete anafikira
muyeso wa bango la mikono isanu ndi umodzi yaikuru. 9Kucindikira
kwa khoma la kuzipinda za m'mphepete kunja kwace kunali
mikono isanu; ndipo mpata wace unali malo olowera m'zipinda za
m'mphepete za kacisi. 10Ndi pakati pa zipinda panali kupingasa
kwa mikono makumi awiri, pozungulira pace ponse pa
nyumba. 11Ndi makomo a zipinda za m'mphepete analoza
kumpatawo, khomo lina kumpoto, ndi lina kumwela; ndi malo a pa
mpatawo anayesa mikono isanu kupingasa kwace pozungulira
pace. 12Ndipo nyumba inali kutsogolo kwa mpata wa mbali ya
kumadzulo inali ya mikono makumi asanu ndi awiri kupingasa
kwace; ndi khoma la nyumbayo pozungulira pace linali la mikono
isanu kucindikira kwace; ndi m'litali mwace mikono makumi asanu
ndi anai. 13Momwemo anayesa kacisi m'litali mwace mikono zana
limodzi; ndi mpatawo, ndi nyumbayo, ndi makoma ace, mikono
zana limodzi; 14kupingasa kwace komwe kwa kukhomo kwa
nyumba, ndi ku mpatawo kum'mawa, mikono zana limodzi.

15Momwemo anayesa m'litali mwace nyumbayo inali kutsogolo
kwace kwa mpata wokhala cakuno cace, ndi makonde ace
am'mwamba, cakuno ndi cauko, mikono zana limodzi, ndi Kacisi wa
m'katimo, ndi makonde a kubwalo; 16ziundo, ndi mazenera a made
okhazikika, ndi makonde am'mwamba akuzinga zipinda
zosanjikizana zao zitatu, pandunji pa ciundo, ocinga ndi matabwa
pozungulira pace, kuyambira pansi kufikira kumazenera; koma
mazenera anaphimbika; 17kufikira pamwamba pa khomo, mpaka
nyumba ya m'katimo, ndi kunja kwace, ndi khoma lonse kwete
m'kati ndi kunja, monga mwa miyeso. 18Ndipo panalembedwapo
ndi akerubi ndi akanjedza, kanjedza pakati pa akerubi; ndi kerubi
ali yense anali ndi nkhope zace ziwiri; 19nkhope ya munthu kuloza
kukanjedza cakuno, ndi nkhope ya mwana wa mkango kuloza
kukanjedza cauko, momwemo m'nyumba monse pozungulira
pace. 20Kuyambira pansi kufikira pamwamba pa khomo
panalembedwa akerubi ndi akanjedza; linatero khoma la
Kacisi. 21Mphuthu za Kacisi zinali zamphwamphwa, ndi
maonekedwe a pakhomo pa malo opatulika ananga maonekedwe a
kacisi. 22Guwa la nsembe linali lamtengo, msinkhu wace mikono
itatu, ndi m'litali mwace mikono iwiri, ndi ngondya zace, ndi tsinde
lace, ndi: thupi, nza mtengo; ndipo ananena ndi ine, Ili ndiko gome
liri pamaso pa Yehova. 23Ndipo Kacisi ndi malo opatulikitsa anali
nazo zitseko ziwiri. 24Ndipo pamakomopo panali zitseko
zopatukana zotembenuzika, cina copatukana pa khomo lina cina
pa linzace. 25Ndipo panalembedwa pamenepo pa Izitseko za Kacisi
akerubi ndi akanjedza, akunga aja adalembedwa pamakhoma;
ndipo panali matabwa ocindikira pakhomo pakhonde
panja, 26Ndipo panali mazenera a made okhazikika, ndi akanjedza
cakuno ndi cauko, kumbali zace za khonde; momwemonso pa
zipinda za m'mphepete mwa nyumba, ndi pa matabwa ocindikira.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Kukonzekanso kwa Kacisi: zipinda zopatulika

1Pamenepo anaturuka nane kumka ku bwalo la kunja, njira ya
kumpoto; nalowa nane ku nyumba yazipinda idali pandunji pa
mpatawo, ndi pandunji pa nyumbayo inaloza kumpoto. 2Cakuno ca
m'litali mwace mwa mikono zana limodzi kunali khomo la kumpoto,
ndi kupingasa kwace mikono makumi asanu. 3Pandunji pa mikono
makumi awiri a bwalo lam'kati, ndi pandunji pa moyalamo mwa
miyala, mwa bwalo lakunja, panali khonde lam'mwamba,
lokomana ndi khonde linzace losanjikika paciwiri. 4Ndi kukhomo
kwa zipinda anakonza poyendapo, kupingasa kwace mikono khumi
m'kati mwace, njira ya mikono zana limodzi, ndi makomo ao
analoza kumpoto. 5Ndipo zipinda zapamwamba zinacepa, pakuti
makonde am'mwamba analanda pamenepo, cifukwa cace
zinacepa koposa zapansi ndi zapakati m'nyumba yazipinda. 6Pakuti
zinasanjikizana pawiri, ndipo zinalibe nsanamira ngati nsanamira
za kumabwalo; cifukwa cace zam'mwambazo zinacepa koposa
zakunsi ndi zapakati kuyambira pansi. 7Ndipo linga linali kunialo,
loli'ngana ndi nyumba yazipinda, kuloza ku bwalo lakunja,
popenyana ndi nyumba yazipinda, m'litali mwace munali mikono
makumi asanu. 8Pakuti kupingasa kwace kwa nyumba yazipinda
inali m'bwalo lakunja, kunali mikono makumi asanu; ndipo taonani,
kuloza ku khomo la Kacisi inali mikono zana limodzi. 9Ndipo pansi
pa zipinda izi panali polowera mbali ya kum'mawa, poloweramo
kucoka ku bwalo lakunja. 10M'kucindikira kwa linga la bwalo, kuloza
kumwera, cakuno ca mpatawo, cakuno ca nyumba, panali nyumba
yazipinda. 11Ndipo njira ya pakhomo pao inanga maonekedwe a
njira ya ku nyumba yazipinda yoloza kumpoto, inalingana nayo
m'litali mwace, momwemonso kupingasa kwace; ndi m'maturukiro
mwace monse munali monga mwa macitidwe a inzace, ndi monga
mwa makomo a inzace. 12Ndi monga mwa makomo a zipinda za
kumwela panali khomo polekeza njira, ndiyo njira yokhudzana ndi
linga la kum'mawa polowamo. 13Pamenepo anati kwa ine, Zipinda
za kumpoto, ndi zipinda za kumwela, ziri cakuno ca mpatawo,
ndizo zipinda zopatulika, kumene ansembe okhala pafupi pa
Yehova azidyera zinthu zopatulikitsa; kumeneko aziika
zopatulikitsa, ndi nsembe yaufa, ndi nsembe yaucimo, ndi nsembe
yoparamula; pakuti malowo ndi opatulika. 14Atalowa ansembe
asaturukenso m'malo opatulika kumka ku bwalo lakunja, koma
komweko aziika zobvala zao zimene atumikira nazo; pakuti ziri
zopatulika; ndipo abvale zobvala zina, nayandikire zinthu wamba
za anthu.
15Atatha tsono kuyesa nyumba ya m'katimo, anaturuka nane njira
ya cipata coloza kum'mawa, nayesa bwalo pozungulira

pace. 16Anayesa mbali ya kum'mawa ndi bango loyesera,
mabango mazana asanu, kuyesa ndi bango loyesera, pozungulira
pace. 17Anayesa mbali ya kumpoto mabango mazana asanu,
kuyesa ndi bango loyesera, pozungulira pace. 18Anayesa mbali ya
kumwela mabango mazana asanu, kuyesa ndi bango
loyesera, 19Anatembenukira ku mbali ya kumadzulo, nayesa
mabango mazana asanu ndi bango loyesera. 20Analiyesa mbali
zace zinai, linali nalo linga pozungulira pace, utali wace mazana
asanu, citando cace mazana asanu, kusiyanitsa pakati pa
zopatulika ndi zawamba.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Kukonzekanso kwa Kacisi: ulemerero wa Mulungu

1Pamenepo anamuka nane ku cipata coloza kum'mawa, 2ndipo
taonani, ulemerero wa Mulungu wa Israyeli unadzera njira ya
kum'mawa, ndi mau ace ananga mkokomo wa madzi ambiri, ndi
dziko linanyezimira ndi ulemerero wace. 3Ndipo maonekedwe a
masomphenya ndinawaona anali monga masomphenya aja
ndinawaona pakudza ine kupasula mudzi; ndi masomphenyawa
anali ngati masomphenya aja ndinawaona ku mtsinje wa Kebara;
ndipo ndinagwa nkhope pansi. 4Ndipo ulemerero wa Yehova
unalowa m'kacisi kudzera njira ya cipata coloza kum'mawa. 5Ndipo
mzimu unandinyamula numuka nane ku bwalo la m'kati; ndipo
taonani, ulemerero wa Mulungu unadzaza kacisi. 6Ndipo ndinamva
wina alikulankhula nane ali m'kacisi, naima nane munthu. 7Ndipo
anati kwa ine, Wobadwa ndi munthu iwe, pano mpokhala mpando
wacifumu wanga, mpoponda ku mapazi anga, pomwe ndidzakhala
pakati pa ana a Israyeli kosatha; ndi nyumba ya Israyeli
siidzadetsanso dzina langa loyera, ngakhale iwo kapena mafumu
ao, mwa cigololo cao, ndi mitembo ya mafumu ao pa misanje
yao, 8ndi kuika ciundo cao pafupi pa ciundo canga, ndi mphuthu
yao pa mbali ya mphuthu yanga, ndipo panali khoma lokha pakati
pa iwo ndi Ine, nadetsa dzina langa loyera ndi zonyansa zao
anazicita; cifukwa cace ndinawatha mu mkwiyo wanga. 9Ataye
tsono cigololo cao ndi mitembo ya mafumu ao kutali kwa Ine,
ndipo ndidzakhala pakati pao kosatha.
10Wabadwa ndi munthu iwe, onetsa nyumba ya Israyeli kacisiyu,
kuti acite manyazi ndi mphulupulu zao; ndipo ayese muyeso
wace. 11Ndipo ngati akacita manyazi nazo zonse anazicita,
uwadziwitse maonekedwe a kacisiyu, ndi muyeso wace, ndi
poturukira pace, ndi polowera pace, ndi malongosoledwe ace onse,
ndi malemba ace onse, ngakhale maonekedwe ace onse, ndi
malamulo ace onse; nuwalembere pamaso pao, kuti asunge
maonekedwe ace onse, ndi malemba ace onse, nawacite. 12Lamulo
la kacisi ndi ili: pamwamba pa phiri malire ace onse pozungulira
pace azikhala opatulikitsa. Taonani, limeneli ndi lamulo la kacisi.
13Ndipo miyeso ya guwa la nsembe, kuyesa mikono ndi iyi:
(mkonowo ndiwo mkono ndi cikhato), tsinde lace likhale mkono,
ndi kupingasa kwace mkono, ndi mkuzi wace m'mphepete mwace
pozungulira pace kuyesa zala; ili ndi tsinde la guwali. 14Ndi
kuyambira kunsi kwace kunthaka, kufikira phaka lamunsi, mikono
iwiri; ndi kupingasa kwace mkono umodzi; ndi kuyambira phaka
laling'ono kufikira phaka lalikuru mikono inai; ndi kupingasa kwace
mkono. 15Ndi guwa lapamwamba mikono inai; ndi pamoto pa guwa
padzaturuka nyanga zinai. 16Ndi pamoto pa guwa, m'litali mwace

mikono khumi ndi iwiri, ndi kupingasa kwace khumi ndi iwiri,
lampwamphwa mbali zace zinai. 17Ndi phaka, m'litali mwace
mikono khumi ndi inai, ndi kupingasa kwace mikono khumi ndi inai
ku mbali zace zinai; ndi mkuzi wace pozungulira pace mkono wa
nusu, ndi tsinde lace mkono pozungulira pace, ndi makwerero ace
aloza kum'mawa.
18Ndipo anati kwa ine, Wobadwa ndi munthu iwe, atero Ambuye
Yehova, Malemba a guwa la nsembe, tsiku lakulimanga,
kuperekapo nsembe zopsereza, ndi kuwazapo mwazi, ndi
awa; 19Upatse ansembe Alevi, a mbeu ya Zadoki, okhala pafupi ndi
Ine, kunditumikira Ine, ati Ambuye Yehova, mwana wa ng'ombe,
akhale wa nsembe yaucimo. 20Nutengeko mwazi wace, ndi kupaka
pa nyanga zinai za guwa, ndi pa ngondya zinai za phaka, ndi pa
mkuzi wace pozungulira; motero uliyeretse ndi kulicitira
cotetezera. 21Utengenso ng'ombe ya nsembe yaucimo, aipsereze
pa malo oikika a kacisi kunja kwa malo opatulika. 22Ndipo tsiku
laciwiri upereke tonde wopanda cirema, akhale nsembe yaucimo;
ndipo ayeretse guwa la nsembe monga umo analiyeretsera ndi
ng'ombeyo. 23Utatha kuliyeretsa upereke mwana wa ng'ombe
wopanda cirema, ndi nkhosa yamphongo ya zoweta yopanda
cirema. 24Ndipo ubwere nazo kwa Yehova, ndi ansembe athirepo
mcere, ndi kuzipereka nsembe yopsereza ya Yehova. 25Masiku
asanu ndi awiri uzikonzera mbuzi tsiku ndi tsiku, ikhale nsembe
yaucimo; akonzerenso mwana wa ng'ombe, ndi nkhosa
yamphongo ya zoweta zopanda cirema. 26Masiku asanu ndi awiri
acite cotetezera guwali ndi kuliyeretsa, momwemo
alipatule. 27Ndipo atatsiriza masiku, kudzacitika tsiku lacisanu ndi
citatu ndi m'tsogolo, ansembe azicita nsembe zanu zopsereza, ndi
nsembe zanu zoyamika pa guwalo; ndipo ndidzakulandirani, ati
Ambuye Yehova.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Kukonzekanso kwa Kacisi: utumiki wa Alevi ndi ansembe

1Pamenepo anandibweza njira ya ku cipata cakunja ca malo
opatulika coloza kum'mawa, koma cinatsekedwa. 2Ndipo Yehova
anati kwa ine, Cipata ici citsekeke, cisatseguke, osalowako
munthu; pakuti Yehova Mulungu wa Israyeli walowerapo; cifukwa
cace citsekeke. 3Koma kunena za kalonga, iye akhale m'menemo
monga kalonga kudya mkate pamaso pa Yehova; alowe ku njira ya
ku khonde la cipata, naturukire njira yomweyi. 4Atatero anamuka
nane njira ya cipata ca kumpoto kukhomo kwa kacisi, ndipo
ndinapenya, taonani, ulemerero wa Yehova unadzaza nyumba ya
Yehova; pamenepo ndinagwa nkhope pansi. 5Ndipo Yehova anati
kwa ine, Wobadwa ndi munthu iwe, samalira bwino, nupenye ndi
maso ako, numve m'makutu mwako zonse ndidzanena nawe,
kunena za malemba onse a nyumba ya Yehova, ndi malamulo ace
onse; nusamalire bwino malowedwe a nyumbayi, ndi maturukidwe
ace onse a malo opatulika. 6Nunene kwa opandukawo, kwa
nyumba ya Israyeli, Atero Ambuye Yehova, Nyumba ya Israyeli inu,
Zikukoleni zonyansa zanu zonse; 7popeza mwalowa nao acilendo
osadulidwa m'mtima, osadulidwa m'thupi akhale m'malo anga
opatulika kuwadetsa, ndiwo nyumba yanga, popereka inu mkate
wanga, mafuta, ndi mwazi; ndipo munatyola pangano langa
pamodzi ndi zonyansa zanu zonse. 8Ndipo simunasunga udikiro wa
zopatulika zanga, koma mwadziikira mokha osunga udikiro wanga
m'malo anga opatulika. 9Atero Ambuye Yehova, Palibe mlendo
wosadulidwa m'mtima, wosadulidwa m'thupi, alowe m'malo anga
opatulika, mwa alendo onse ali pakati pa ana a Israyeli. 10Koma
Aleviwo anandicokera kumka kutariwo, posokera Israyeli, amene
anandisokerera ndi kutsata mafano ao, iwowa adzasenza
mphulupulu yao. 11Koma adzakhala atumiki m'malo anga
opatulika, akuyang'anira ku zipata za kacisi, ndi kutumikira
m'kacisimo, aziwaphera anthu nsembe yopsereza, ndi nsembe
yophera naime pamaso pao kuwatumikira. 12Popeza
anawatumikira pamaso pa mafano ao, nakhala cokhumudwitsa ca
mphulupulu ca nyumba ya Israyeli, cifukwa cace ndawakwezera
dzanja langa, ati Ambuye Yehova; ndipo adzasenza mphulupulu
yao. 13Ndipo asayandikire kwa Ine kundigwirira nchito ya nsembe,
kapena kuyandikira zopatulika zanga ziri zonse zopatulikitsazo;
koma azisenza manyazi ao, ndi zonyansa zao anazicita. 14Koma
ndidzawaika akhale osunga udikiro wa kacisi kwa utumiki wace
wonse, ndi zonse zakumacitika m'mwemo.
15Koma ansembe Alevi, ana a Zadoki, akusunga udikiro wa malo
anga opatulika pondisokerera ana a Israyeli, iwowa
adzandiyandikira kunditumikira Ine, nadzaima pamaso panga,

kupereka mafuta ndi mwazi kwa Ine, ati Ambuye Yehova; 16iwowa
adzalowa m'malo anga opatulika, nadzayandikira ku gome langa
kunditumikira, nadzasunga udikiro wanga. 17Ndipo kudzatero,
polowa iwo ku zipata za bwalo lam'kati abvale zobvala zabafuta;
koma zaubweya asazibvale ponditumikira Ine m'zipata za bwalo la
m'kati, ndi m'kacisi. 18Akhale nao akapa abafuta pamitu pao, ndi
akabudula m'cuuno mwao; asabvale m'cuuno kanthu kali konse
kakucititsa thukuta. 19Ndipo akaturukira ku bwalo lakunja, ku bwalo
lakunja kuti anthu, azibvula zobvala zao zimene atumikira nazo,
naziike m'zipinda zopatulika, nabvale zobvala zina; angapatule
anthu ndi zovala zao. 20Ndipo asamete mitu yao, kapena
asalekerere nzera za tsitsi lao zikule, azingosenga mitu
yao. 21Kungakhale kumwa vinyo, wansembe asamwe polowa ku
bwalo la m'katimo. 22Kungakhale kutenga amasiye kapena
osudzulidwa akhale akazi ao, asacite; koma atenge anamwali a
mbeu ya nyumba ya Israyeli, kapena wamasiye ndiye wamasiye
wa wansembe. 23Ndipo aziphunzitsa anthu anga asiyanitse pakati
pa zopatulika ndi zinthu wamba, ndi kuwazindikiritsa pakati pa
zodetsa ndi zoyera. 24Ndipo pakakhala mlandu, aimeko kuweruza;
auweruze monga mwa maweruzo anga, ndipo azisunga malamulo
anga, ndi malemba anga, pa madyerero anga onse oikika;
napatulikitse masabata anga. 25Ndipo asayandikire kwa munthu ali
yense wakufa, angadzidetse; koma cifukwa ca atate, kapena mai,
kapena mwana wamwamuna, kapena mwana wamkazi, kapena
mbale, kapena mlongo wopanda mwamuna, nkuloleka
kudzidetsa. 26Ndipo atayeretsedwa amwerengere masiku asanu
ndi awiri. 27Ndipo tsiku loti alowa m'malo opatulika, bwalo lam'kati,
kutumikira m'malo opatulika, apereke nsembe yace yaucimo, ati
Ambuye Yehova. 28Ndipo adzakhala naco colowa; Ine ndine colowa
cao; musawapatsa colandira cao m'Israyeli; Ine ndine colandira
cao. 29Azidya nsembe yaufa, ndi nsembe yaucimo, ndi nsembe
yoparamula; ndipo ziri zonse zoperekedwa ciperekere m'Israyeli
ndi zao. 30Ndi zoyamba za zipatso zoyamba za zinthu ziri zonse,
ndi nsembe za kweza ziri zonse za nsembe zanu zonse zokweza
nza ansembe; muperekenso ufa wanu woyamba kwa wansembe,
kuti mdalitso ukhalebe pa nyumba yako. 31Ansembe asadyeko
kanthu kakufa kokha, kapena kogwidwa ndi cirombo, ngakhale
mbalame, kapena nyama.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Cigawo ca dziko

1Ndipo pogawa dziko likhale calowa cao, mupereke copereka kwa
Yehova, ndico gawo lopatulika la dziko; m'litali mwace likhale la
mabango zikwi makumi awiri mphambu zisanu, ndi kupingasa
kwace zikwi makumi awiri; likhale lopatulika m'malire ace onse
pozungulira pace. 2Kutengako malo opatulika akhale nayo mikono
mazana asanu m'litali mwace, ndi mazana asanu kupingasa
kwace, lamphwamphwa pozungulira pace; ndi pabwalo pace
poyera pozungulira pace mikono makumi asanu. 3Ndipo kuyambira
poyesedwapo uyese zikwi makumi awiri mphambu zili sanu m'litali
mwace, ndi zikwi khumi kupingasa kwace; m'menemo ndimo
mukhale malo opatulika, ndiwo opatulika, ndiwo
opatulikitsa. 4Ndilo gawo lopatulika la dziko, ndilo la ansembe
atumiki a malo opatulika, amene ayandikira kutumikira Yehova;
apo ndipo amange nyumba zao, likhale malo a pa okha a: kwa
malo opatulika. 5Ndipo zikwi makumi awiri mphambu zisanu
m'litali mwace, ndi zikwi khumi kupingasa kwace, ndilo gawo la
Alevi, atumiki a kacisi; likhale lao lao la midzi yokhalamo. 6Ndipo
dziko lace la mudziwo mulipereke la zikwi zisanu kupingasa kwace,
ndi zikwi makumi awiri mphambu zisanu m'litali mwace, pa mbali
ya cipereko copatulika, ndilo la nyumba yonse ya Israyeli. 7Ndipo
kalonga adzakhala nalo gawo lace mbali yina ndi mbali inzace ya
cipereko copatulika, ndi ya dziko la mudzi, kutsogolo kwa cipereko
copatulika, ndi kutsogolo kwa dziko la mudzi, mbali ya kumadzulo
kumadzulo, ndi mbali ya kum'mawa kum'mawa; ndi m'litali mwace
mudzalingana ndi limodzi la magawo, kuyambira ku malire a
kumadzulo kufikira malire a kum'mawa. 8M'dzikomo ili lidzakhala
lace lace m'Israyeli; ndipo akalonga anga sadzazunzanso anthu
anga, koma adzapereka dziko kwa nyumba ya Israyeli monga mwa
mapfuko ao.
9Atero Ambuye Yehova, Likufikireni akalonga a Israyeli inu, lekani
kucita ciwawa, ndi kulanda za eni ace; mucite ciweruzo ndi
cilungamo; lekani kupitikitsa anthu anga m'zolowa zao, ati Ambuye
Yehova. 10Muzikhala nayo miyeso yoona, ndi efa woona, ndi bati
loona. 11Efa ndi bati zikhale za muyeso umodzi, bati liyese limodzi
la magawo khumi la homeri, efa lomwe liyese limodzi la magawo
khumi la homeri; muyeso wao uyesedwa monga mwa
homeri. 12Ndipo sekeli ndilo magera makumi awiri; masekeli
makumi awiri, ndi masekeli awiri ndi asanu, ndi masekeli khumi ndi
asanu, ndiwo mane wanu. 13Copereka mucipereke ndico limodzi la
magawo asanu ndi limodzi la efa, kulitapa pa homeri wa tirigu;
muperekenso limodzi la magawo asanu ndi limodzi la efa, kulitapa
pa homeri wa barele; 14ndi gawo lonenedwa la mafuta, la bati wa

mafuta, ndilo limodzi la magawo khumi la bati, kulitapa pa kori;
ndiwo mabati khumi, ndiwo homeri; pakuti mabati khumi ndiwo
homeri; 15ndi mwana wa nkhosa mmodzi wa zoweta, kumtenga pa
mazana awiri wocokera ku madimba a Israyeli, ndiye wa nsembe
yaufa, ndi wa nsembe yopsereza, ndi wa nsembe zoyamika,
kuwacitira cotetezera, ati Ambuye Yehova. 16Anthu onse a m'dziko
azipereka copereka ici cikhale ca kalonga wa m'Israyeli. 17Ndipo
udindo wa kalonga ndiwo kupereka nsembe zopsereza, ndi nsembe
zaufa, ndi nsembe zothira, pamadyerero, ndi pokhala mwezi, ndi
pamasabata; pa madyerero onse oikika a nyumba ya Israyeli;
ndipo apereke nsembe yaucimo, ndi nsembe yaufa, ndi nsembe
yopsereza, ndi nsembe zamtendere, kucitira cotetezera nyumba ya
Israyeli.

Nsembe ya pa mwezi woyamba

18Atero Ambuye Yehova, Mwezi woyamba, tsiku loyamba la mwezi,
uzitenga mwana wa ng'ombe wopanda cirema, ndipo uyeretse
malo opatulika. 19Ndipo wansembe atengeko mwazi wa nsembe
yaucimo, naupake pa mphuthu za kacisi, ndi pa ngondya zinai za
phaka la guwa la nsembe, ndi pa mphuthu za cipata ca bwalo
lam'kati. 20Tsiku lacisanu ndi ciwiri la mweziwo ucitire momwemo
ali yense wolakwa ndi wopusa; motero mucitire kacisiyo
comtetezera.

Za Paskha

21Mwezi woyamba, tsiku lakhumi ndi cinai la mwezi, muzicita
Paskha, madyerero a masiku asanu ndi awiri; audye mkate
wopanda cotupitsa. 22Ndipo tsiku lomwelo kalonga adzikonzere
yekha ndi anthu onse a m'dziko ng'ombe, ikhale ya nsembe
yaucimo. 23Ndipo masiku asanu ndi awiri a madyerero akonzere
Yehova nsembe yopsereza, ng'ombe zisanu ndi ziwiri, ndi nkhosa
zamphongo zisanu ndi ziwiri zopanda cirema, tsiku ndi tsiku,
masiku asanu ndi awiriwa; ndi tonde tsiku ndi tsiku, akhale wa
nsembe yaucimo. 24Nakonze nsembe yaufa, ku ng'ombe kukhale
efa; ndi ku nkhosa yamphongo kukhale efa; ndi kuefa kukhale hini
wa mafuta. 25Mwezi wacisanu ndi ciwiri, tsiku lakhumi ndi cisanu la
mwezi, pamadyerero, acite momwemo masiku asanu ndi awiri,
monga mwa nsembe yaucimo, monga mwa nsembe yopsereza, ndi
monga mwa nsembe yaufa, ndi monga mwa mafuta.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Za Sabata ndi pokhala mwezi

1Atero Ambuye Yehova, Pa cipata ca bwalo lam'kati coloza
kum'mawa patsekedwe masiku asanu ndi limodzi ogwira nchito;
koma tsiku la Sabata patsegulidwe, ndi tsiku lokhala mwezi
patsegulidwe. 2Ndipo kalonga azilowera njira ya ku khonde la
cipataco, kunja kwace, naime ku nsanamira ya cipata; ndipo
ansembe akonze nsembe yace yopsereza, ndi nsembe zace
zoyamika, nalambire iye ku ciundo ca cipata; atatero aturuke;
koma pacipata pasatsekedwe mpaka madzulo. 3Ndipo anthu a
m'dziko alambire pa citseko ca cipata ici pamaso pa Yehova
pamasabata, ndi pokhala mwezi. 4Ndipo nsembe yopsereza imene
kalonga azipereka kwa Yehova pa Sabata ndiyo ana a nkhosa
asanu ndi mmodzi opanda cirema, ndi nkhosa yamphongo
yopanda cirema, 5ndi nsembe yaufa ikhale efa wa pa nkhosa
yamphongo, ndi nsembe ya ufa wa pa ana a nkhosa, monga
akhoza kupatsa; ndi hini a wa mafuta wa paefa. 6Ndipo nsembe ya
tsiku lokhala mwezi ikhale mwana wa ng'ombe wopanda cirema,
ndi ana a nkhosa asanu ndi mmodzi, ndi nkhosa yamphongo,
zikhale zopanda cirema; 7ndipo akonze nsembe yaufa, efa wa pa
ng'ombe, ndi efa wa pa nkhosa yamphongo, ndi pa ana a nkhosa,
monga akhoza; ndi hini wa mafuta wa paefa. 8Ndipo polowa
kalonga azilowera njira ya ku khonde la cipata, naturuke njira
yomweyo.

Malangizo a popereka nsembe

9Koma pofika anthu a m'dziko pamaso pa Yehova m'madyerero
oikika, iye amene alowera njira ya ku cipata ca kumpoto
kudzalambira, aturukire njira ya ku cipata ca kumwera; ndi iye
amene alowera njira ya ku cipata ca kumwera, aturukire njira ya ku
cipata ca kumpoto; asabwerere njira ya cipata anadzeraco, koma
aturukire m'tsogolo mwace. 10Kalongayo tsono, polowa iwo alowe
pakati pao, ndipo poturuka iwo aturukire pamodzi. 11Ndi
pamadyerero, ndi pa masiku opatulika, nsembe yaufa ikhale ya efa
wa pa ng'ombe, ndi efa wa pa nkhosa yamphongo, ndi pa ana a
nkhosa, monga akhoza kupatsa; ndi hini wa mafuta wa
paefa. 12Ndipo kalonga akapereka copereka caufulu nsembe
yopsereza, kapena nsembe zoyamika kwa Yehova, amtsegulire pa
cipata coloza kum'mawa; ndipo azipereka nsembe yace yopsereza,
ndi nsembe zace zoyamika, monga umo amacitira tsiku la Sabata;
atatero aturuke; ndipo ataturuka, wina atseke
pacipata. 13Uziperekanso kwa Yehova mwana wa nkhosa wa caka
cimodzi akhale nsembe yopsereza wopanda cirema, tsiku ndi tsiku,
m'mawa ndi m'mawa, uzimpereka. 14Uperekenso nsembe yaufa
pamodzi naye m'mawa ndi m'mawa, limodzi la magawo asanu ndi

limodzi la efa, ndi limodzi la magawo atatu la hini wa mafuta,
kusanganiza ndi ufa wosalala, ndiyo nsembe yaufa ya Yehova
kosalekeza, mwa lemba losatha. 15Momwemo apereke mwana wa
nkhosa, ndi nsembe yaufa, ndi mafuta, m'mawa ndi m'mawa,
nsembe yopsereza kosalekeza.

Mapatsidwe a kalonga

16Atero Ambuye Yehova, Kalonga akapatsa mwana wace wina
wamwamuna mphatso idzakhala colowa cace, ndico cao cao ca
ana ace, colowa cao. 17Koma akapatsa mphatso yotenga ku colowa
cace kwa wina wa anyamata ace, idzakhala yace mpaka caka ca
ufulu; pamenepo ibwerere kwa kalonga, koma colowa cace cikhale
ca ana ace. 18Ndipo kalonga asatengeko colowa ca anthu
kuwazunza, ndi kulanda dziko lao lao; apatse ana ace colowa
kulemba dziko lace lace, kuti anthu anga asabalalike, yense kucoka
m'dziko lace.

Pophikira ansembe

19Pamenepo anapita ndi ine podzera paja pali ku mbali ya cipata
kumka ku zipinda zopatulika za ansembe zoloza kumpoto; ndipo
taonani, kunali malo cauko kumadzulo. 20Ndipo anati kwa ine, Pano
ndipo ansembe aziphikira nsembe yoparamula, ndi nsembe
yaucimo; kumenenso azioca mikate ya ufa wa nsembe, kuti
asaturuke nazo ku bwalo lakunja ndi kupatulikitsa
anthu, 21Pamenepo anaturukira nane ku bwalo lakunja,
nandipititsa ku ngondya zinai za bwaloli; ndipo taonani, m'ngondya
monse munali bwalo. 22M'ngondya zinai za bwalo munali mabwalo
ocingika, m'litali mwace mikono makumi anai, kupingasa kwace
makumi atatu; awa anai m'ngondyazi analingana muyeso
wace. 23Ndipo panali maguwa pozungulira pace m'menemo,
pozungulira pace pa mabwalo anai; ndipo anamanga maguwawo
ndi mafuwa pansi pace pozungulirapo. 24Ndipo anati kwa ine, Izi
ndi nyumba zophikiramo, kumene atumiki a kacisi aziphikira
nsembe ya anthu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masomphenya a madzi oturuka m'Kacisi watsopano

1Ndipo anandibwezera ku khomo la nyumba, ndipo taonani, panatumphuka madzi pansi pa ciundo ca nyumba kum'mawa; pakuti khomo lace la nyumba linaloza kum'mawa; ndipo madzi anatsika kucokera pansi pa nyumba, ku mbali ya lamanja lace, kumwela kwa guwa la nsembe. 2Pamenepo anaturuka nane njira ya ku cipata ca kumpoto, nazungulira nane njira yakunja kumka ku cipata cakunja, njira ya ku cipata coloza kum'mawa; ndipo taonani, panaturuka madzi pa mbali ya kulamanja. 3Poturuka munthuyu kumka kum'mawa ndi cingwe coyesera m'dzanja lace, anayesa mikono cikwi cimodzi, nandipititsa pamadzi, madzi oyesa m'kakolo. 4Nayesanso cikwi cimodzi, nandipititsa pamadzi, madzi oyesa m'maondo. Nayesanso cikwi cimodzi, nandipititsa pamadzi, madzi oyesa m'cuuno. 5Atatero anayesanso cikwi cimodzi, ndipo mtsinje wosakhoza kuoloka ine, popeza madzi adakula, madzi osambira, mtsinje wosaoloka munthu. 6Ndipo anati kwa ine, Wobadwa ndi munthu iwe, waona ici? Nanditenga kundikwezetsa ndi mtsinje. 7Nditabwera tsono, taonani, pa gombe la mtsinjewo mitengo yambirimbiri tsidya lino ndi lija. 8Pamenepo anati kwa ine, Madzi awa aturukira ku dera la kum'mawa, natsikira kucidikha, nayenda kunyanja; atathira kunyanja akonzeka madzi ace. 9Ndipo kudzatero kuti zamoyo zonse zocuruka zidzakhala ndi moyo kuti konse mtsinjewo ufikako, ndi nsomba zidzacuruka kwambiri; pakuti madzi awa anafikako, nakonzeka madzi a m'nyanja; ndipo kuli konse mtsinje ufikako ziri zonse zidzakhala ndi moyo. 10Ndipo kudzacitika, kuti asodzi adzaima komweko; kuyambira pa Engedi kufikira ku Eneglaimu kudzakhala poyanikira makoka; nsomba zao zidzakhala za mitundu mitundu, ngati nsomba za m'nyanja yaikuru, zambirimbiri. 11Koma pali matope ace ndi zithaphwi zace sipadzakonzeka, paperekedwa pakhale pamcere. 12Ndipo kumtsinje, kugombe kwace tsidya lino ndi lija, kudzamera mtengo uli wonse wa cakudya, osafota tsamba lace, zipatso zace zomwe zosasowa; idzabala zipatso zatsopano mwezi ndi mwezi, popeza madzi ace atumphuka m'malo opatulika; ndi zipatso zace zidzakhala cakudya, ndi tsamba lace lakuciritsa.

Malire a dziko

13Atero Ambuye Yehova, Malire amene mugawe nao dziko likhale colowa cao monga mwa mafuko khumi ndi awiri a Israyeli ndi awa: Yosefe akhale nao magawo awiri. 14Ndipo mudzakhala nalo colowa canu wina ndi mnzace yemwe, ndilo limene ndinakwezapo dzanja langa kulipereka kwa makolo anu, ndi dziko ili lidzakugwerani colowa canu. 15Ndipo malire a dzikoli ndi awa: mbali ya kumpoto, kuyambira ku nyanja yaikuru, kutsata njira ya ku Heteloni, kufikira

polowera ku Zedadi; 16Hamati, Berota, Sibraimu, ndiwo pakati pa
malire a Damasiko, ndi malire a Hamati; Hazere Hatikoni ndiwo ku
malire a Haurani. 17Ndi malire ocokera kunyanja ndiwo
Hazaremoni, ku malire a Damasiko, ndi kumpoto kulinga kumpoto
kuli malire a Hamati, Ndiyo mbali ya kumpoto. 18Ndi mbali ya
kum'mawa pakati pa Haurani, ndi Damasiko, ndi Gileadi, ndi dziko
la Israyeli, ndiwo Yordano; muyese kuyambira malire a kumpoto
kufikira nyanja ya kum'mawa. Ndiyo mbali ya kum'mawa. 19Ndi
mbali ya kumwela kuloza kumwela ndiyo kuyambira ku Tamara
kufikira ku madzi a Meriboti Kadesi, ku mtsinje wa Aigupto, ndi ku
nyanja yaikuru. Ndiyo mbali ya kumwela kuloza kumwela. 20Ndi
mbali ya kumadzulo ndiyo nyanja yaikuru, kuyambira malire a
kumwela kufikira pandunji polowera ku Hamati. Ndiyo mbali ya
kumadzulo.
21Motero mudzigawire dziko ili monga mwa mafuko a
Israyeli. 22Ndipo kudzacitika kuti muligawe ndi kucita maere,
likhale colowa canu, ndi ca alendo akukhala pakati pa inu; ndipo
akhale kwa inu ngati obadwa m'dziko mwa ana a Israyeli, alandire
colowa pamodzi ndi inu mwa mafuko a Israyeli. 23Ndipo kudzatero
kuti kupfuko kumene mlendo akhalako kumeneko mumpatse
colowa cace, ati Ambuye Yehova.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Magawidwe a dziko mwa mafuko khumi ndi awiri

1Maina a mafuko tsono ndi awa: Kuyambira nsonga ya kumpoto, ku
mbali ya njira ya ku Heteloni, polowera ku Hamati, Hazarenani ku
malire a Damasiko kumpoto, ku mbali ya ku Hamati; ndi mbali zace
zilinge kum'mawa ndi kumadzulo; Dani akhale nalo gawo
limodzi. 2Ndi m'malire a Dani, kuyambira mbali ya kum'mawa
kufikira mbali ya kumadzulo; Aseri, limodzi. 3Ndi m'malire a Aseri,
kuyambira mbali ya kum'mawa kufikira mbali ya kumadzulo;
Nafitali, limodzi. 4Ndi m'malire a Nafitali, kuyambira mbali ya
kum'mawa kufikira mbali ya kumadzulo; Manase, limodzi. 5Ndi
m'malire a Manase, kuyambira mbali ya kum'mawa kufikira mbali
ya kumadzulo; Efraimu, limodzi. 6Ndi m'malire a Efraimu,
kuyambira mbali ya kum'mawa kufikira mbali ya kumadzulo;
Rubeni, limodzi. 7Ndi m'malire a Rubeni, kuyambira mbali ya
kum'mawa kufikira mbali ya kumadzulo; Yuda, limodzi.
8Ndi m'malire a Yuda, kuyambira mbali ya kum'mawa kufikira
mbali ya kumadzulo, pakhale copereka a mucipereke, mabango
zikwi makumi awiri mphambu zisanu kupingasa kwace, ndi m'litali
mwace lilingane ndi magawo enawo, kuyambira mbali ya
kum'mawa kufikira mbali ya kumadzulo; ndi malo opatulika akhale
pakati pace. 9Copereka mucipereke kwa Yehova cikhale ca
mabango zikwi makumi awiri mphambu zisanu m'litali mwace, ndi
zikwi khumi kupingasa kwace. 10Ndipo m'mwemo mudzakhala
copereka copatulika ca ansembe kumpoto, zikwi makumi awiri
mphambu zisanu a m'litali mwace, ndi kumadzulo zikwi khumi
kupingasa kwace, ndi kum'mawa zikwi khumi kupingasa kwace, ndi
kumwela zikwi makumi awiri mphambu zisanu m'litali mwace; ndi
pakati pace pakhale malo opatulika a Yehova. 11Cidzakhala ca
ansembe opatulidwa a ana a Zadoki, amene anasunga udikiro
wanga osasokera, muja anasokera ana a Israyeli, ndi muja
anasokera Alevi. 12Ndi ciperekoco cikhale cao cotapa pa copereka
ca dziko, ndico copatulikitsa pa malire a Alevi. 13Ndipo polingana
ndi malire a ansembe Alevi akhale nalo gawo la zikwi makumi awiri
mphambu zisanu m'litali mwace, ndi zikwi khumi kupingasa kwace;
m'litali mwace monse ndimo zikwi makumi awiri mphambu zisanu,
ndi kupingasa kwace zikwi khumi. 14Ndipo asagulitseko, kapena
kulisintha, kapena kupitiriza zipatso zoyamba za dziko; pakuti liri
lopatulika la Yehova. 15Ndipo zikwi zisanu zotsalazo m'kupingasa
kwace, cakuno ca zikwi makumi awiri mphambu zisanu, zikhale za
nchito wamba za mudzi, za kumangapo zapabusa; ndi mudzi
ukhale pakati pace. 16Ndi miyeso yace ndi iyi: mbali ya kumpoto,
mabango zikwi zinai mphambu mazana asanu; ndi mbali ya
kumwela, zikwi zinai mphambu mazana asanu; ndi mbali ya

kummawa, zikwi zinai mphambu mazana asanu; ndi mbali ya kumadzulo, zikwi zinai mphambu mazana asanu. 17Ndipo mudziwo ukhale ndi busa lace; kumpoto mabango mazana awiri mphambu makumi asanu, kumwela mazana awiri mphambu makumi asanu, ndi kum'mawa mazana awiri mphambu makumi asanu, ndi kumadzulo mazana awiri mphambu makumi asanu. 18Ndipo madera otsalawo m'litali mwace alingane ndi copereka copatulika, ndico zikwi khumi kum'mawa, ndi zikwi khumi kumadzulo, alingane ndi copereka copatulika; ndi zipatso zace zikhale za cakudya ca iwo ogwira nchito m'mudzi. 19Iwo ogwira nchito m'mudzi mwa mafuko onse a Israyeli alimeko. 20Copereka conse ndico mabango zikwi makumi awiri mphambu zisanu m'litali mwace, zikwi makumi awiri mphambu zisanu kupingasa kwace; mucipereke copereka copatulika camphwamphwa, pamodzi ndi dziko la mudziwo. 21Ndipo madera ena otsalawo ndiwo a kalonga, mbali yina ndi yina ya copereka copatulika ndi ya dziko la mudzi, kutsogolo kwa zikwi makumi awiri mphambu zisanu za copereka ku malire a kum'mawa, ndi kumadzulo kutsogolo kwa zikwi makumi awiri mphambu zisanu ku malire a kumadzulo, pandunji pa magawo enawo ndiwo ca kalonga; ndipo copereka copatulika ndi malo opatulika a kacisi zidzakhala pakati pace. 22Kuyambira tsono dziko la Alevi kufikira dziko la mudzi, ndiwo a pakati pa magawo ace a kalonga, pakati pa malire a Yuda ndi malire a Benjamini, kukhale kwa kalonga.
23Kunena za mafuko otsala tsono, kuyambira ku mbali ya kum'mawa kufikita mbali ya kumadzulo, Benjamini akhale nalo gawo limodzi. 24Ndi ku malire a Benjamini, kuyambira mbali ya kum'mawa kufikira mbali ya kumadzulo; Simeoni, gawo limodzi. 25Ndi ku malire a Simeoni kuyambira mbali ya kum'mawa kufikira mbali ya kumadzulo; Isakara, limodzi. 26Ndi ku malire a Isakara, kuyambira mbali ya kum'mawa kufikira mbali ya kumadzulo; Zebuloni, limodzi. 27Ndi ku malire a Zebuloni, kuyambira ku mbali ya kum'mawa kufikira mbali ya kumadzulo; Gadi, limodzi. 28Ndi ku malire a Gadi, mbali ya kumwela, kuloza kumwela, malire akhale kuyambira ku Tamara kufikira ku madzi a Meribati ndi Kadesi, ku mtsinje wa Aigupto, kufikira ku nyanja yaikuru. 29Ili ndi dziko muligawire mafuko a Israyeli ndi kucita maere, likhale colowa cao; ndipo awa ndi magawo ao, ati Ambuye Yehova.
30Ndipo malekezero a mudzi ndi awa: mbali ya kumpoto avese mabango zikwi zinai mphambu mazana asanu; 31ndi zipata za mudzi zidzakhala monga mwa maina a mafuko a Israyeli; zipata zitatu kumpoto: cipata cimodzi ca Rubeni, cipata cimodzi ca Yuda, cipata cimodzi ca Levi; 32ndi ku mbali ya kum'mawa zikwi zinai

mphambu mazana asanu, ndi zipata zitatu: cipata cimodzi ca Yosefe, cipata cimodzi ca Benjamini, cipata cimodzi ca Dani; 33ndi ku mbali ya kumwela ayese zikwi zinai mphambu mazana asanu, ndi zipata zitatu: cipata cimodzi ca Simeoni, cipata cimodzi ca Isakara, cipata cimodzi ca Zebuloni; 34ku mbali ya kumadzulo zikwi zinai mphambu mazana asanu, ndi zipata zace zitaru; cipata cimodzi ca Gadi, cipata cimodzi ca Aseri, cipata cimodzi ca Nafitali. 35Pozungulira pace ndipo mabango zikwi khumi mphambu zisanu ndi zitatu, ndi dzina la mudziwo kuyambira tsiku ilo lidzakhala, Yehova ali pomwepo.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Yeremiya acita nkhawa, adziponya kwa Yehova

1Ine ndine munthuyu wakuona msauko ndi ndodo ya ukali wace.
2Wanditsogolera, nandiyendetsa mumdima, si m'kuunika ai.
3Zoonadi amandibwezera-bwezera dzanja lace monditsutsa tsiku lonse.
4Wagugitsa thupi langa ndi khungu langa, natyola mafupa anga.
5Wandimangira zitando za nkhondo, wandizinga ndi ulembe ndi mabvuto.
6Wandikhalitsa mumdima ngati akufakale.
7Wanditsekereza ndi guta, sindingaturuke; walemeretsa unyolo wanga.
8Inde, popfuula ine ndi kuitana andithandize amakaniza pemphero langa.
9Watsekereza njira zanga ndi miya la yosema, nakhotetsa mayendedwe anga.
10Andikhalira cirombo colalira kapena mkango mobisalira.
11Wapambutsa njira zanga, nanding'amba; nandipululutsa.
12Wathifula uta wace, nandiyesa polozetsa mubvi.
13Walowetsa m'imso mwanga mibvi ya m'phodo mwace.
14Ndasanduka wondiseka mtundu wanga wonse, ndi nyimbo yao tsiku lonse.
15Wandidzaza ndi zowawa, wandikhutitsa civumulo.
16Watyolanso mano anga ndi tinsangalabwi, wandikuta ndi phulusa.
17Watarikitsanso moyo wanga ndi mtendere; ndinaiwala zabwino.
18Ndipo ndinati, Mphamvu yanga yatha, osayembekezanso kanthu kwa Yehova.
19Kumbukirani msauko Wanga ndi kusocera kwanga, ndizo civumulo ndi ndulu.
20Moyo wanga uzikumbukirabe nuwerama mwa ine,
21Ndiri naco ciyembekezo popeza ndilingalira ici ndiyembekeza kanthu.
22Cifukwa cakusathedwa ife ndico cifundo ca Yehova, pakuti cisoni cace sicileka;
23Cioneka catsopano m'mawa ndi m'mawa; mukhulupirika ndithu.
24Moyo wanga uti, Gawo langa ndiye Yehova; cifukwa cace ndidzakhulupirira.
25Yehova akhalira wabwino omlindirira, ndi moyo womfunafuna.
26Nkokoma kuti munthu ayembekeze ndi kulindirira modekha cipulumutso ca Yehova.
27Nkokoma kuti munthu asenze gori ali wamng'ono.
28Akhale pa yekha, natonthole, pakuti Mulungu wamsenzetsa ilo.
29Aike kamwa lace m'pfumbi; kapena ciripo ciyembekezo.
30Atembenuzire wompanda tsaya lace, adzazidwe ndi citonzo.

31Pakuti Yehova sadzataya kufikira nthawi zonse,
32Angakhale aliritsa, koma adzacitira cisoni monga mwa kucuruka kwa zifundo zace.
33Pakuti samasautsa dala, ngakhale kumvetsa ana a anthu cisoni.
34Kupondereza andende onse a m'dziko,
35Kupambutsa ciweruzo ca munthu pamaso pa Wam'mwambamwamba,
36Kukhotetsa mlandu wa munthu, zonsezi Ambuye sazikonda.
37Ndani anganene, conena cace ndi kucitikadi, ngati Ambuye salamulira?
38Kodi m'kamwa mwa Wam'mwambamwamba simuturuka zobvuta ndi zabwino?
39Kodi munthu wamoyo adandauliranji pokhala m'zocimwa zace?
40Tisanthule ntiyese njira zathu ntibwerenso kwa Yehova.
41Titukulire mitima yathu ndi, manja athu omwe kwa Mulungu ali kumwamba.
42Ife tilakwa ndi kupikisana nanu, ndipo Inu simunatikhululukira.
43Mwadzikuta ndi mkwiyo ndi kutilondola, mwatipha osacitira cisoni.
44Mwadzikuta ndi mtambo kuti pemphero lathu lisapyolemo.
45Mwatiika pakati pa amitundu ngati zinyalala ndi za kudzala.
46Adani athu onse anatiyasamira,
47Mantha ndi dzenje zitifikira, ndiphokose ndi cionongeko.
48M'diso mwanga mutsikamitsinje ya madzi cifukwa ca mwana wamkazi wa anthu amtundu wanga woonongedwa,
49Diso langa lingotsanulira osaleka, osapumula,
50Kufikira Yehova adzazolika kumwamba ndi kuona;
51Diso langa limvetsa moyo wanga zowawa cifukwa ca ana akazi onse a m'mudzi mwanga.
52Ondida opanda cifukwa anandiinga ngati mbalame;
53Anaononga moyo wanga m'dzenje, naponya mwala pamwambapaine;
54Madzi anayenda pamwamba pa mutu panga, ndinati, dalikhidwa.
55Ndinaitana dzina lanu, Yehova, ndiri m'dzenje lapansi;
56Munamva mau anga; musabise khutu lanu popuma ndi popfuulaine.
57Munayandikira tsiku la kukuitanani ine; munati, Usaope.
58Ambuye munanenera moyo wanga mirandu yace; munaombola moyo wanga.
59Yehova, mwaona coipa anandicitiraco, mundiweruzire;
60Mwaona kubwezera kwao konse ndi zopangira zao zonse za pa ine.
61Mwamva citonzo cao, Yehova, ndi zopangira zao zonse za pa ine,

62Milomo ya akutsutsana nane ndi zolingalira zao za pa ine tsiku
lonse.
63Taonani kukhala ndi kunyamuka kwao; ndine nyimbo yao.
64Mudzawabwezera cilango, Yehova, monga mwa macitidwe a
manja ao;
65Muphimbe mtima wao ndi kuwatemberera;
66Mudzawalondola mokwiya ndi kuwaononga pansi pa thambo la
Yehova.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Tsoka a anthu Avuda

1Ha! golidi wagugadi; golidi woona woposa wasandulika;
Miyala ya malo opatulika yakhutulidwa pa malekezero a makwalalaonse.
2Ana a Ziyoni a mtengo wapatari, olingana ndi golidi woyengetsa,
Angoyesedwa ngati mbiya zadothi zozipanga manja a woumba.
3Angakhale ankhandwe amapatsa bere, nayamwitsa ana ao;
Koma mwana wamkazi wa anthu amtundu wanga wasanduka wankhanza, ngati nthiwatiwa za m'cipululu.
4Lilime la mwana woyamwa limamatira kumalakalaka kwace ndi ludzu;
Ana ang'ono apempha mkate koma palibe wakuwanyemera.
5Omwe anadya zolongosoka angosiyidwa m'makwalala;
Omwe analeredwa nabvekedwa mlangali afungatira madzala.
6Pakuti mphulupulu ya mwana wamkazi wa anthu amtundu wanga, ikula koposa cimo la Sodomu,
Umene unapasuka m'kamphindi, anthu osaucitira kanthu.
7Omveka ace anakonzeka koposa cipale cofewa, nayera koposa mkaka,
Matupi ao anafiira koposa timiyala toti pyu; maonekedwe ao ananga a safiro wa mtengo wapatari.
8Maonekedwe ao ada koposa makala, sazindikirika m'makwalala;
Khungu lao limamatira pa mafupa ao, lakhwinyata, lasanduka ngati ndodo.
9Ophedwa ndi lupanga amva bwino kupambana ophedwa ndi njala;
Pakuti amenewa angokwalika napyozedwa, posowa zipatso za m'munda.
10Manja a akazi acisoni anaphika anaanao;
Anali cakudya cao poonongeka mwana wamkazi wa anthu a mtundu wanga.
11Yehova wakwaniritsa kuzaza kwace, watsanulira ukali wace;
Anayatsa moto m'Ziyoni, unanyambita maziko ace,
12Mafumu a dziko lapansi sanakhulupirira, ngakhale onse okhala kunja kuno,
Kuti adani ndi amaliwongo adzalowadi m'zipata za Yerusalemu.
13Ndico cifukwa ca macimo a aneneri ndi mphulupulu za ansembeace,
Amene anakhetsa mwazi wa olungama pakati pace.
14Asocera m'makwalala ngati akhungu, aipsidwa ndi mwazi;
Anthu sangakhudze zobvala zao.
15Amapfuula kwa iwo, Cokani, osakonzeka inu, cokani, cokani, musakhudze kanthu.

Pothawa iwo ndi kusocera, anthu anati mwa amitundu,
Sadzagoneranso kuno.
16Mkwiyo wa Yehova unawalekanitsa, sadzawasamaliranso;
Iwo sanalemekeza ansembe, sanakomera mtima akulu.
17Maso athu athedwa, tikali ndi moyo, poyembekeza thandizo cabe;
Kudikira tinadikira mtundu wosatha kupulumutsa.
18Amalondola mapazi athu, sitingayende m'makwalala athu;
Citsiriziro cathu cayandikira, masiku athu akwaniridwa; pakuti citsiriziro cathu cafikadi.
19Otilondola anaposa ziombankhanga za m'mlengalenga m'liwilo lao,
Anatithamangitsa pamapiri natilalira m'cipululu.
20Wodzozedwa wa Yehova, ndiye mpweya wa m'mphuno mwathu, anagwidwa m'maenje ao; Amene tinanena kuti, Tidzakhala m'mthunzi mwace pakati pa amitundu,
21Kondwera nusangalale, mwana wamkazi wa Edomu, wokhala m'dzikola Uzi;
Cikho cidzapita ngakhale mwa iwenso; udzaledzera ndi kubvulazako.
22Mphulupulu yako yatha, mwana wamkazi wa Ziyoni, Yehova sadzakutenganso ndende;
Koma adzazonda mphulupulu yako, mwana wa mkazi wa Edomu, nadzabvumbulutsa zocimwa zako.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Maliro 5

Adandaulira Yehova pa tsoka la ukapolo wao

1Yehova, kumbukirani cotigweraci,
Penyani nimuone citonzo cathu.
2Colowa cathu casanduka ca alendo,
Ndi nyumba zathu za acilendo.
3Ndife amasiye opanda atate,
Amai athu akunga akazi amasiye.
4Tinamwa madzi athu ndi ndalama,
Tiona nkhuni zathu pozigula.
5Otilondola atigwira pakhosi pathu,
Tatopa osaona popumira.
6Tinagwira mwendo Aigupto
Ndi Asuri kuti tikhute zakudya.
7Atate athu anacimwa, kulibe iwo;
Ndipo tanyamula mphulupulu zao.
8Akapolo atilamulira;
Palibe wotipulumutsa m'dzanja lao.
9Timalowa m'zoopsya potenga zakudya zathu,
Cifukwa ca lupanga la m'cipululu,
10Khungu lathu lapserera ngati pamoto
Cifukwa ca kuwawa kwa njala.
11Anaipitsa akazi m'Ziyoni,
Ndi anamwali m'midzi ya Yuda.
12Anawapacika akalonga manja ao;
Sanalemekeza nkhope za akulu.
13Anyamata ananyamula mphero,
Ana nakhumudwa posenza nkhuni.
14Akulu adatha kuzipata,
Anyamata naleka nyimbo zao.
15Cimwemwe ca mtima wathu calekeka,
Masewera athu asanduka maliro.
16Korona wagwa pamutu pathu;
Kalanga ife! pakuti tinacimwa.
17Cifukwa ca ici mtima wathu ufoka,
Cifukwa ca izi maso athu acita cimbuuzi;
18Pa phiri la Ziyoni lopasukalo
Ankhandwe ayendapo.
19Inu, Yehova, mukhala cikhalire,
Ndi mpando wanu wacifumu ku mibadwo mibadwo.
20Bwanji mutiiwala ciiwalire,
Ndi kutisiya masiku ambirimbiri;
21Mutitembenuzire kwa Inu, Yehova, ndipo tidzatembenuzidwadi,
Mukonzenso masiku athu ngati kale lija.

22Koma mwatikaniza konse,
Mwatikwiyira kopambana.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Daniel

Danieli 1

Maleredwe a Danieli ndi anzace kwa mfumu ya ku Babulo

1CAKA cacitatu ca Yehoyakimu mfumu ya Yuda, Nebukadinezara
mfumu ya ku Babulo adadza ku Yerusalemu, naumangira misasa
ya nkhondo. 2Ndipo Yehova anapereka Yehoyakimu mfumu ya
Yuda, m'dzanja lace, pamodzi ndi zipangizo zina za m'nyumba ya
Mulungu, namuka nazo iye ku dziko la Sinara, ku nyumba ya
mulungu wace, nalonga zipangizozo m'nyumba ya cuma ca
mulungu wace. 3Ndipo mfumu inauza Asipenazi mkuru wa adindo
kuti abwere nao ena a ana a Israyeli, a mbeu ya mafumu, ndi ya
akalonga; 4anyamata opanda cirema, a maonekedwe okoma, a
luso la nzeru zonse, ocenjera m'kudziwa, a luntha lakuganizira,
okhoza kuimirira m'cinyumba ca mfumu; ndi kuti awaphunzitse
m'mabuku, ndi manenedwe a Akasidi. 5Ndipo mfumu inawaikira
gawo la cakudya ca mfumu tsiku ndi tsiku, ndi la vinyo wakumwa
iye, ndi kuti awalere zaka zitatu, kuti potsiriza pace aimirire
pamaso pa mfumu. 6Mwa awa tsono munali a ana a Yuda, Danieli,
Hananiya, Misayeli, ndi Azariya. 7Ndi mkuru wa adindo anawapatsa
maina ena; Danieli anamucha Belitsazara; ndi Hananiya, Sadrake;
ndi Misaeli, Mesaki; ndi Azariya, Abedinego. 8Koma Danieli
anatsimikiza mtimti kuti asadzidetse ndi cakudya ca mfumu,
kapena ndi vinyo amamwa; cifukwa cace anapempha mkuru wa
adindo amlole asadzidetse. 9Ndipo Mulungu anamkometsera
Danieli mtima wa mkuru wa adindo, amcitire cifundo. 10Nati mkuru
wa adindo kwa Danieli. Ine ndiopa mbuyanga mfumu, amene
anakuikirani cakudya canu ndi cakumwa canu; pakuti aonerenji
nkhope zanu zacisoni zoposa za anyamata olingana ndi inu?
momwemo mudzaparamulitsa mutu wanga kwa mfumu. 11Nati
Danieli kwa kapitao, amene mkuru wa adindo adamuikayo
ayang'anire Danieli, Hananiya, Misaeli, ndi Azariya, 12Muyesetu
anyamata anu masiku khumi; atipatse zomera m'nthaka tidye, ndi
madzi timwe. 13Pamenepo mupenye maonekedwe athu ndi
maonekedwe a anyamata akudya cakudya ca mfumu; ndi monga
umo muonera, mucitire anyamata anu. 14Ndipo anawamvera mau
awa, nawayesa masiku khumi. 15Atatha masiku khumiwo tsono,
anaona kuti maonekedwe ao ndi kunenepa kwao anaposa
anyamata onse adadyawo zakudya za mfumu. 16Pamenepo
kapitaoyo anacotsa cakudya cao ndi vinyo akadamwa, nawapatsa
zomera m'nthaka. 17Koma anyamata amene anai, Mulungu
anawapatsa cidziwitso ndi luntha la m'mabuku ali onse, ndi nzeru;
koma Danieli anali nalo luntha la m'masomphenya ndi maloto
onse. 18Atatha masiku inanenawo mfumu kuti alowe nao, mkulu wa

adindo analowa nao pamaso pa Nebukadinezara. 19Ndipo mfumu
inalankhula nao, koma mwa iwo onse sanapezeka monga Danieli,
Hananiya, Misaeli, ndi Azariya; naimirira iwo pamaso pa
mfumu. 20Ndipo m'mau ali onse anzeru ndi aluntha, amene mfumu
inawafunsira, inawapeza akuposa alembi ndi openda onse
m'ufumu wace wonse. 21Nakhala moyo Danieli mpaka caka
coyamba ca Koresi.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Nebukadinezara alota, Danieli ammasulira lotolo

1Caka caciwiri ca Nebukadinezara mfumu, Nebukadinezarayo
analota maloto, ndi mzimu wace unabvutika, ndi tulo tace
tidamwazikira. 2Pamenepo mfumu inauza munthu aitane alembi,
ndi openduza, ndi aula, ndi Akasidi, amuululire mfumu maloto ace.
Nalowa iwo, naimirira pamaso pa mfumu. 3Niti nao mfumu,
Ndalota loto, nubvutika mzimu wanga kudziwa lotolo. 4Pamenepo
Akasidi anati kwa mfumu m'Ciaramu, Mfumu, mukhale ndi moyo
cikhalire: mufotokozere anyamata anu lotoli, ndipo tidzakuuzani
kumasulira kwace. 5Niyankha mfumu, niti kwa Akasidi,
Candicokera cinthuci; mukapanda kundidziwitsa lotoli ndi
tanthauzo lace, mudzadulidwa nthuli nthuli, ndi nyumba zanu
zidzayesedwa dzala. 6Koma mukandidziwitsa lotoli, ndi kumasulira
kwace, mudzalandira kwa ine mphatso, ndi mphotho, ndi ulemu
waukuru; cifukwa cace mundidziwitse lotoli ndi kumasulira
kwace. 7Nabwerezanso iwo kuyankha, nati, Mfumu ifotokozere
anyamata ace lotoli, ndipo tidzaidziwitsa kumasulira
kwace. 8Mfumu inayankha, niti, Ndidziwatu kuti mukunkhuniza
dala, pakuona inu kuti cinthuci candicokera. 9Koma mukapanda
kundidziwitsa lotoli, mlandu wanu ndi umodzi; popeza
mwapanganiranatu mau onama ndi oipa, kuwanena pamaso
panga, mpaka idzasanduka nyengo; cifukwa cace mundifotokozere
lotoli, momwemo ndidzadziwa kuti mudzandidziwitsa kumasulira
kwace komwe. 10Akasidi anayankha pamaso pa mfumu, nati,
Palibe munthu pa dziko lapansi wokhoza kuulula mlandu wa
mfumu; cifukwa cace palibe mfumu, mkuru, kapena wolamulira,
wafunsira cinthu cotere kwa mlembi, kapena wopenduza, kapena
Akasidi ali onse. 11Pakuti cinthu acifuna mfumu ncapatali; ndipo
palibe wina wokhoza kuciulula pamaso pa mfumu, koma milungu
imene kwao sikuli pamodzi ndi anthu. 12Cifukwa cace mfumu
inakwiya, nizaza kwambiri, nilamulira kuti awaphe anzeru onse
m'Babulo. 13M'mwemo cilamuliroco cidamveka, ndi eni nzeru adati
aphedwe; anafuna-funanso Danieli ndi anzace
aphedwe. 14Pamenepo Danieli anabweza mau a uphungu wanzeru
kwa Arioki mkuru wa olindirira a mfumu, adaturukawo kukapha eni
nzeru a ku Babulo; 15anayankha nati kwa Arioki mkuru wa
olindirira a mfumu, Cilamuliro ca mfumu cifulumiriranji? Pamenepo
Arioki anadziwitsa Danieli cinthuci. 16Nalowa Danieli, nafunsa
mfumu amuikire nthawi, kuti aululire mfumu kumasulira kwace.
17Pamenepo Danieli anapita ku nyumba kwace, nadziwitsa anzace
Hananiya, Misaeli, ndi Azariya, cinthuci; 18kuti apemphe zacifundo
kwa Mulungu wa Kumwamba pa cinsinsi ici; kuti Danieli ndi anzace
asaonongeke pamodzi ndi eni nzeru ena a ku Babulo. 19Pamenepo

cinsinsico cinabvumbulutsidwa kwa Danieli m'masomphenya a usiku. Ndipo Danieli analemekeza Mulungu wa Kumwamba. 20Danieli anayankha, nati, Lilemekezedwe dzina la Mulungu ku nthawi za nthawi, a pakuti nzeru ndi mphamvu ziri zace; 21pakuti amasanduliza nthawi ndi nyengo, acotsa mafumu, nalonga mafumu, apatsa anzeru nzeru, ndi cidziwitso kwa iwo okhoza kuzindikira. 22Iye abvumbulutsa zinthu zakuya ndi zinsinsi; adziwa zokhala mumdima, ndi kuunika kumakhala kwa Iye. 23Ndikuyamikani ndi kukulemekezani Inu, Mulungu wa makolo anga, pakuti mwandipatsa nzeru ndi mphamvu; ndipo mwandidziwitsa tsopano ici tacifuna kwa Inu; pakuti mwatidziwitsa mlandu wa mfumu. 24Potero Danieli analowa kwa Arioki amene mfumu idamuika aononge eni nzeru a ku Babulo; anamuka, natero naye, Usaononga eni nzeru a ku Babulo, undilowetse kwa mfumu, ndipo ndidzaululira mfumu kumasulirako. 25Pamenepo Arioki analowa naye Danieli kwa mfumu mofulumira; natero nayo, Ndapeza munthu wa ana a ndende a Yuda, ndiye adzadziwitsa mfumu kumasulira kuja. 26Mfumu inayankha, niti kwa Danieli, amene dzina lace ndiye Belitsazara, Ukhoza kodi kundidziwitsa lotolo ndidalilota, ndi kumasulira kwace? 27Nayankha Danieli pamaso pa mfumu, nati, Cinsinsi inacitira liuma mfumu, angakhale anzeru, openduza, alembi, kapena alauli, sakhoza kuciululira mfumu; 28koma kuli Mulungu Kumwamba wakubvumbulutsa zinsinsi; Iye ndiye wadziwitsa mfumu Nebukadinezara cimene cidzacitika masiku otsiriza. Loto lanu, ndi masomphenya a m'mtima mwanu pakama panu, ndi awa: 29Inu mfumu, maganizo anu analowa m'mtima mwanu muli pakama panu, akunena za ico cidzacitika m'tsogolomo; ndipo Iye amene abvumbulutsa zinsinsi wakudziwitsani codzacitikaco. 30Koma ine, cinsinsi ici sicinabvumbulutsidwa kwa ine cifukwa ca nzeru ndiri nayo yakuposa wina ali yense wamoyo, koma kuti kumasuliraku kudziwike kwa mfumu, ndi kuti mudziwe maganizo a mtima wanu. 31Inu mfumu munapenya ndi kuona fano lalikuru. Fanoli linali lalikuru, ndi kunyezimira kwace kunaposa; linali kuima popenyana ndi inu, ndi maonekedwe ace anali oopsa, 32Pano ili tsono, mutu wace unali wagolidi wabwino, cifuwa cace ndi manja ace zasiliva, mimba yace ndi cuuno cace zamkuwa, 33miyendo yace yacitsulo, mapazi ace mwina citsulo mwina dongo. 34Munali cipenyere kufikira mwala unasemedwa popanda manja, umene unagunda fanoli pa mapazi ace okhala citsulo ndi dongo, nuwaphwanya. 35Pamenepo citsulo, dongo, mkuwa, siliva, ndi golidi, zinapereka pamodzi, nizinasanduka ngati mungu wa pa madwale a malimwe; ndi mphepo inaziuluza, osapezekanso malo ao; ndi mwala udagunda fanowo unasanduka phiri lalikuru,

nudzaza dziko lonse lapansi. 36Ili ndi loto; kumasulira kwace tsono
tikufotokozerani mfumu. 37Inu mfumu ndinu mfumu ya mafumu,
pakuti Mulungu wa Kumwamba anakupatsani ufumu, ndi mphamvu
yaikuru, ndi ulemu; 38ndipo pali ponse pokhala ana a anthu Iye
anapereka nyama za kuthengo, ndi mbalame za m'mlengalenga,
m'dzanja lanu; nakucititsani ufumu pa izi zonse; inu ndinu mutuwo
wagolidi. 39Ndi pambuyo pa inu padzauka ufumu wina wocepa ndi
wanu, ndi ufumu wina wacitatu wamkuwa wakucita ufumu pa dziko
lonse lapansi. 40Ndi ufumu wacinai udzakhala wolimba ngati
citsulo, popeza citsulo ciphwanya ndi kufoketsa zonse; ndipo
monga citsulo ciswa zonsezi, uwu udzaphwanya ndi
kuswa. 41Ndipo umo mudaonera mapazi ndi zala zace, mwina
dongo la woumba, mwina citsulo; ufumuwo udzakhala
wogawanika, koma momwemo mudzakhala mphamvu ya citsulo;
popeza mudaona citsulo cosanganizika ndi dongo. 42Ndi zala za
mapazi, mwina citsulo ndi mwina dongo, momwemo ufumuwo,
mwina wolimba mwina wogamphuka. 43Ndi umo mudaonera
citsulo cosanganizika ndi dongo, iwo adzadzisokoneza ndi ana a
anthu wamba; koma sadzapharikizana, monga umo citsulo
sicimasanganizikana ndi dongo. 44Ndipo masiku a mafumu aja
Mulungu wa Kumwamba adzaika ufumu woti sudzao nongeka ku
nthawi zonse, ndi ulamuliro wace sudzasiyidwira mtundu wina wa
anthu, koma udzaphwanya ndi kutha maufumu ao onse
nudzakhala cikhalire. 45Umo mudaonera kuti mwala unasemedwa
m'phiri popanda manja, ndi kuti udapera citsulo, mkuwa, dongo,
siliva, ndi golidi; Mulungu wamkuru wadziwitsa mfumu cidzacitika
m'tsogolomo; lotoli nloona, ndi kumasulira kwace
kwakhazikika. 46Pamenepo mfumu Nebukadinezara anagwa
nkhope yace pansi, nalambira Danieli, nati amthirire nsembe yaufa
ndi ya zonunkhira zokoma. 47Mfumu inamyankha Danieli, niti,
Zoona Mulungu wako ndiye Mulungu wa milungu, ndi Mbuye wa
mafumu, ndi wobvumbulutsa zinsinsi; popeza wakhoza
kubvumbulutsa cinsinsi ici. 48Pamenepo mfumu inasandutsa
Danieli wamkuru, nimpatsa mphatso zazikuru zambiri,
namlamuliritsa dera lonse la ku Babulo; nakhala iye kazembe
wamkuru wa anzeru onse a ku Babulo. 49Pamenepo Danieli
anapempha mfumu, ndipo anaika Sadrake, Mesake, ndi Abedinego,
ayang'anire nchito za dera la ku Babulo. Koma Danieli anakhala
m'bwalo la mfumu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Nebukadinezara apanga fano lagolidi

1Mfumu Nebukadinezara anapanga fano lagolidi, msinkhu wace
mikono makumi asanu ndi limodzi, ndi thunthu lace mikono isanu
ndi umodzi; analiimika pa cidikha ca Dura, m'dera la ku
Babulo. 2Ndipo mfumu Nebukadinezara inatumiza kukasonkhanitsa
akalonga, akazembe, ndi ziwanga, oweruza, akulu osunga cuma,
mandoda, ankhoswe, ndi olamulira onse a madera, abwere
kuzurula fanoli adaliimika mfumu Nebukadinezara. 3Pamenepo
akalonga, akazembe, ndi ziwanga, oweruza, akulu osunga cuma,
mandoda, ankhoswe, ndi olamulira onse a madera, anasonkhanira
kupereka fano adaliimika mfumu Nebukadinezara, naimirira
pamaso pa fano adaliimika Nebukadinezara. 4Ndipo wolalikira
anapfuulitsa, kuti, Akulamulirani inu anthu, mitundu ya anthu a
manenedwe osiyana, 5kuti pakumva inu mau a lipenga, citoliro,
zeze, sansi, cisakasa, ngoli, ndi zoyimbitsa ziri zonse, mugwadire
ndi kulambira fano lagolidi adaliimika mfumu
Nebukadinezara; 6ndipo ali yense wosagwadira ndi kulambira,
adzaponyedwa nthawi yomweyo m'kati mwa ng'anjo yotentha
yamoto. 7Potero nthawi yomweyo pakumva anthu onse mau a
lipenga, citoliro, zeze, sansi, cisakasa, ndi zoyimbitsa ziri zonse,
anthu onse, mitundu ya anthu a manenedwe osiyana, anagwadira,
nalambira fano lagolidi adaliimika mfumu
Nebukadinezara. 8Cifukwa cace anayandikira Akasidi ena nthawi
yomweyi, naneneza Ayuda. 9Anayankha, nati kwa mfumu
Nebukadinezara, Mfumu, mukhale ndi moyo cikhalire. 10Inu mfumu
mwalamulira kuti munthu ali yense amene adzamva mau a
lipenga, citoliro, zeze, sansi, cisakasa, ngoli, ndi zoyimbitsa ziri
zonse, agwadire, nalambire fanolo lagolidi; 11ndi yense
wosagwadira ndi kulambiraadzaponyedwa m'kati mwa ng'anjo
yotentha yamoto. 12Alipo Ayuda amene munawaika ayang'anire
nchito ya dera la ku Babulo, Sadrake, Mesake, ndi Abedinego,
amuna awa, mfumu, sanasamalira inu, satumikira milungu yanu,
kapena kulambira fano lagolidi mudaliimikalo.

Anzace a Danieli aponyedwa m'ng'anjo yamoto

13Pamenepo Nebukadinezara, mumkwiyo ndi m'ukali wace,
anawauza abwere nao Sadrake, Mesake, ndi Abedinego. Ndipo
anabwera nao amunawa kwa mfumu. 14Nebukadinezara
anayankha, nati kwa iwo, Kodi mutero dala, Sadrake, Mesake, ndi
Abedinego, kusatumikira milungu yanga, ndi kusalambira fano
lagolidi ndinaliimikalo? 15Mukabvomereza tsono, pakumva mau a
lipenga, citoliro, zeze, sansi, cisakasa, ndi ngoli, ndi zoyimbitsa ziri
zonse, kugwadira ndi kulambira fano ndinalipanga, cabwino; koma
mukapanda kulambira, mudzaponyedwa nthawi yomweyi m'kati

mwa ng'anjo yotentha yamoto; ndipo mulungu amene adzakulanditsani m'manja mwanga ndani? 16Sadrake, Mesake, ndi Abedinego, anayankha, nati kwa mfumu Nebukadinezara, Sikufunika kuti tikuyankheni pa mlandu uwu. 17Taonani, Mulungu wathu amene timtumikira akhoza kutilanditsa m'ng'anjo yotentha yamoto, nadzatilanditsa m'dzanja lanu, mfumu. 18Koma akapanda kutero, dziwani, mfumu, kuti sitidzatumikira milungu yanu, kapena kulambira fano lagolidi mudaliimikalo. 19Pamenepo Nebukadinezara anadzazidwa ndi ukali, ndi maonekedwe a nkhope yace anasandulikira Sadrake, Mesake, ndi Abedinego; anayankha, nati asonkheze ng'anjo kasanu ndi kawiri koposa umo amasonkhezera. 20Nauza amuna ena amphamvu a m'khamu lace la nkhondo amange Sadrake, Mesake, ndi Abedinego, ndi kuwaponya m'ng'anjo yotentha yamoto. 21Pamenepo amuna awa anamangidwa ali cibvalire zopfunda zao, maraya ao, ndi nduwira zao, ndi zobvala zao zina; naponyedwa m'kati mwa ng'anjo yotentha yamoto. 22Motero, popeza mau a mfumu anafulumiza, ndi ng'anjo inatentha koposa, lawi la moto linapha iwo aja ananyamula Sadrake, Mesake, ndi Abedinego. 23Ndipo amuna atatu awa, Sadrake, Mesake, ndi Abedinego, anagwa pansi omangidwa m'kati mwa ng'anjo yotentha yamoto. 24Pamenepo mfumu Nebukadinezara anadabwa, nauka msanga, nanena nati kwa mandoda ace, Kodi sitinaponya amuna atatu omangidwa m'kati mwa moto? Anayankha nati kwa mfumu, Inde mfumu. 25Anayankha, nati, Taonani, ndirikuona amuna anai omasuka, alikuyenda m'kati mwa moto; ndipo alibe kuphwetekwa, ndi maonekedwe a wacinai akunga mwana wa milungu. 26Pamenepo Nebukadinezara anayandikira pa khomo la ng'anjo yotentha yamoto, analankhula, nati, Sadrake, Mesake, ndi Abedinego, inu atumiki a Mulungu Wam'mwambamwamba, turukani, idzani kuno. Pamenepo Sadrake, Mesake, ndi Abedinego, anaturuka m'kati mwa moto. 27Ndipo akalonga, akazembe, ndi ziwanga, ndi mandoda a mfumu, atasonkhana, anaona amuna awa, kuti moto unalibe mphamvu pa matupi ao, losawauka tsitsi la pamutu pao, ndi zopfunda zao zosasandulika, pfungo lomwe lamoto losawaomba. 28Nebukadinezara ananena, nati, Alemekezedwe Mulungu wa Sadrake, Mesake, ndi Abedinego, amene anatuma mthenga wace, napulumutsa atumiki ace omkhulupirira Iye, nasanduliza mau a ine mfumu, napereka matupi ao kuti asatumikire kapena kulambira mulungu wina yense, koma Mulungu wao wao. 29Cifukwa cace ndilamulira kuti anthu ali onse, mtundu uli wonse, ndi a manenedwe ali onse, akunenera molakwira Mulungu wa Sadrake, Mesake, ndi Abedinego, adzadulidwa nthuli nthuli, ndi nyumba zao zidzasanduka dzala;

popeza palibe mulungu wina akhoza kulanditsa motero. 30Pamenepo mfumu inakuza Sadrake, Mesake, ndi Abedinego, m'dera la ku Babulo.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Loto la Nebukadinezara la mtengo waukuru

1Mfumu Nebukadinezara, kwa anthu, mitundu ya anthu, ndi a
manenedwe okhala pa dziko lonse lapansi: Mtendere ucurukire
inu. 2Candikomera kuonetsa zizindikilo ndi zozizwa, zimene
anandicitira Mulungu Wam'mwambamwamba. 3Ha! zizindikilo zace
nzazikuru, ndi zozizwa zace nza mphamvu, ufumu wace ndiwo
ufumu wosatha, ndi kulamulira kwace ku mibadwo mibadwo.
4Ine Nebukadinezara ndinalimkupumula m'nyumba mwanga, ndi
kukhala mwaufulu m'cinyumba canga, 5Ndinaona loto lakundiopsa,
ndi zolingilira za pakama panga, ndi masomphenya a m'mtima
mwanga, zinandibvuta ine. 6Cifukwa cace ndinalamulira kuti adze
kwa ine anzeru onse a ku Babulo, kuti andidziwitse kumasulira
kwace kwa lotoli. 7Pamenepo anafika alembi, openda, Akasidi, ndi
alauli; ndipo ndinawafotokozera lotoli, koma sanandidziwitsa
kumasulira kwace. 8Koma potsiriza pace analowa pamaso panga
Danieli, dzina lace ndiye Belitsazara, monga mwa dzina la mulungu
wanga, amenenso muli mzimu wa milungu yoyera m'mtima
mwace; ndipo ndinamfotokozera lotoli pamaso pace, ndi
kuti, 9Belitsazara iwe, mkuru wa alembi, popeza ndidziwa kuti mwa
iwe muli mzimu wa milungu yoyera, ndi kuti palibe cinsinsi
cikusautsa, undifotokozere masomphenya a loto langa ndalotali,
ndi kumasulira kwace. 10Masomphenya a m'mtima mwanga
pakama panga ndi awa: Ndinapenya ndi kuona mtengo pakati pa
dziko lapansi, msinkhu wace ndi waukuru. 11Mtengowo unakula,
nulimba, ndi msinkhu wace unafikira kumwamba, nuonekera
mpaka cilekezero ca dziko lonse lapansi. 12Masamba ace anali
okoma, ndi zipatso zace zinacuruka, ndi m'menemo munali
zakudya zofikira onse, nyama za kuthengo zinatsata mthunzi
wace, ndi mbalame za m'mlengalenga zinafatsa m'thambi zace,
ndi nyama zonse zinadyako. 13Ndinaona m'masomphenya a
m'mtima mwanga pakama panga, taonani, mthenga woyera
anatsika kumwamba. 14Anapfuulitsa, natero, Likhani mtengowo,
sadzani nthambi zace, yoyolani masamba ace, mwazani zipatso
zace, nyama zicoke pansi pace, ndi mbalame pa nthambi
zace. 15Koma siyani citsa ndi mizu yace m'nthaka, comangidwa ndi
mkombero wa citsulo ndi mkuwa, mu msipu wa kuthengo;
ncokhathamira ndi mame a kumwamba, ndi gawo lace likhale
pamodzi ndi nyama ziri m'macire a m'dziko. 16Mtima wace
usandulike, usakhalenso mtima wa munthu, apatsidwe mtima
wonga wa nyama, nizimpitire nthawi zisanu ndi ziwiri. 17Citsutso ici
adacilamulira amithenga oyerawo, anacifunsa, nacinena, kuti
amoyo adziwe kuti Wam'mwambamwamba alamulira m'ufumu wa
anthu, naupereka kwa ali yense Iye afuna, nauutsira wolubukira

anthu. 18Loto ili ndinaliona ine mfumu Nebukadinezara; ndipo iwe,
Belitsazara, undifotokozere kumasulira kwace, popeza anzeru onse
a m'ufumu wanga sakhoza kundidziwitsa kumasulira kwace; koma
iwe ukhoza, popeza mwa iwe muli mzimu wa milungu yoyera.

Danieli ammasulira lotolo

19Pamenepo Danieli, dzina lace ndiye Belitsazara anadabwa
nthawi, namsautsa maganizo ace. Mfumu inayankha, niti,
Belitsazara, lisakusautse lotoli, kapena kumasulira kwace.
Belitsazara anayankha, nati, Mbuye wanga, lotoli likadakhala la iwo
akudana nanu, ndi kumasulira kwace kwa iwo akuutsana
nanu. 20Mtengo mudauona umene unakula, nukhala wolimba,
nufikira kumwamba msinkhu wace, nuonekera pa dziko lonse
lapansi, 21umene masamba ace anali okoma, ndi zipatso zace
zocuruka, ndi m'menemo munali cakudya cofikira onse, umene
nyama za kuthengo zinakhala pansi pace, ndi mbalame za
m'mlengalenga zinapeza pokhala pao pa nthambi yace; 22ndinu,
mfumu; mwakula, mwalimba, pakuti ukulu wanu wakula, nufikira
kumwamba, ndi ufumu wanu ku cilekezero ca dziko
lapansi. 23Tsono, kuti mfumu inaona mthenga woyera wotsika
kumwamba, ndi kuti, Likhani mtengowo ndi kuuononga, koma
siyani citsa cace ndi mizu m'nthaka, comangidwa ndi mkombero
wa citsulo ndi mkuwa, mu msipu wa kuthengo, nicikhale
cokhathamira ndi mame a kumwamba, ndi gawo lace likhale
pamodzi ndi nyama za kuthengo, mpaka zitampitira nthawi zisanu
ndi ziwiri; 24kumasulira kwace ndi uku, mfumu; ndipo cilamuliro ca
Wam'mwambamwamba cadzera mbuye wanga mfumu: 25kuti
adzakuingitsani kukucotsani kwa anthu, ndi pokhala panu
padzakhala pamodzi ndi nyama za kuthengo; ndipo mudzadya
udzu ngati ng'ombe, nimudzakhala wokhathamira ndi mame a
kumwamba, nizidzakupitirani nthawi zisanu ndi ziwiri, mpaka
mudzadziwa kuti Wam'mwambamwamba alamulira m'ufumu wa
anthu, naupereka kwa ali yense Iye afuna mwini. 26Ndipo kuti
anauza asiye citsa ndi mizu ya mtengo, ufumu wanu
udzakhazikikira inu, mukakatha kudziwa kuti Kumwamba
kumalamulira. 27Cifukwa cace, mfumu, kupangira kwanga
kukomere inu, dulani macimo anu ndi kucita cilungamo, ndi
mphulupulu zanu mwa kucitira aumphawi cifundo; kuti kapena
nthawi ya mtendere wanu italike.

Nebukadinezara acita misala

28Conseci cinagwera mfumu Nebukadinezara. 29Itatha miyezi
khumi ndi iwiri, analikuyenda m'cinyumba cacifumu ca ku
Babulo. 30Mfumu inanena, niti, Suyu Babulo wamkuru
ndinammanga, akhale pokhala pacifumu, ndi mphamvu yanga
yaikuru uoneke ulemerero wa cifumu canga? 31Akali m'kamwa

mwa mfumu mau awa, anamgwera mau ocokera kumwamba, ndi kuti, Mfumu Nebukadinezara, anena kwa iwe: ufumu wakucokera. 32Nadzakuinga kukucotsa kwa anthu, ndi pokhala pako udzakhala pamodzi ndi nyama za kuthengo; adzakudyetsa udzu ngati ng'ombe; nizidzakupitira nthawi zisanu ndi ziwiri, mpaka udzadziwa kuti Wam'mwambamwamba alamulira m'ufumu wa anthu, naupereka kwa ali yense Iye afuna mwini. 33Nthawi yomweyo anacitika mau awa kwa Nebukadinezara; anamuinga kumcotsa kwa anthu; nadya udzu ngati ng'ombe iye, ndi thupi lace linakhathamira ndi mame a kumwamba, mpaka tsitsi lace lidamera ngati nthenga za ciombankhanga ndi makadabo ace ngati makadabo a mbalame. 34Atatha masiku awa tsono, ine Nebukadinezara ndinakweza maso anga kumwamba, ndi nzeru zanga zinandibwerera; ndipo ndinalemekeza Wam'mwambamwamba, ndi kumyamika ndi kumcitira ulemu Iye wokhala cikhalire; pakuti kulamulira kwace ndiko kulamulira kosatha, ndi ufumu wace ku mibadwo mibadwo; 35ndi okhala pa dziko lapansi onse ayesedwa acabe; ndipo Iye acita mwa cifunito cace m'khamu la kumwamba ndi mwa okhala pa dziko lapansi; ndipo palibe woletsa dzanja lace, kapena wakunena naye, Mucitanji? 36Nthawi yomweyi nzeru zanga zinandibwerera, ndi cifumu canga ndi kunyezimira kwanga zinandibwerera, kuti uonekenso ulemerero wa ufumu wanga; ndi mandoda anga ndi akuru anga anandifuna; ndipo ndinakhazikika m'ufumu wanga, Iye nandioniezeranso ukulu wocuruka. 37Tsono ine Nebukadinezara ndiyamika, ndi kukuza, ndi kulemekeza Mfumu ya Kumwamba, pakuti nchito zace zonse nzoona, ndi njira zace ciweruzo; ndi oyenda m'kudzikuza kwao, Iye akhoza kuwacepetsa.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Madyerero a Belisazara, dzanja lolemba pakhoma

1Mfumu Belisazara anakonzera anthu ace akulu cikwi cimodzi
madyerero akuru, namwa vinyo pamaso pa cikwico. 2Belisazara,
pakulawa vinyo, anati abwere nazo zotengera za golidi ndi siliva
adazicotsa Nebukadinezara atate wace ku Kacisi ali ku Yerusalemu,
kuti mfumu ndi akuru ace, akazi ace ndi akazi ace ang'ono,
amweremo. 3Nabwera nazo zotengera zagolidi adazicotsa ku Kacisi
wa nyumba ya Mulungu ya ku Yerusalemu, ndipo mfumu ndi akuru
ace, akazi ace ndi akazi ace ang'ono, anamweramo. 4Anamwa
vinyo, nalemekeza milungu yagolidi, ndi yasiliva, yamkuwa,
yacitsulo, yamtengo, ndi yamwala. 5Nthawi yomweyo zinabuka
zala za dzanja la munthu, nizinalemba pandunji pa coikapo nyali,
pomata pa khoma la cinyumba ca mfumu; ndipo mfumu inaona
nsonga yace ya dzanja lidalembalo. 6Pamenepo padasandulika pa
nkhope pace pa mfumu, ndi maganizo ace anamsautsa, ndi
mfundo za m'cuuno mwace zinaguruka, ndi maondo ace
anaombana. 7Nipfuulitsa mfumu abwere nao openda, Akasidi, ndi
alauli, Mfumu inalankhula, niti kwa anzeru a ku Babulo, Ali yense
amene adzawerenga lemba ili, nadzandifotokozera kumasulira
kwace, adzabvekedwa cibakuwa, ndi unyolo wagolidi m'khosi
mwace, nadzakhala wolamulira wacitatu m'ufumuwu. 8Pamenepo
analowa anzeru onse a mfumu, koma sanakhoza kuwerenga
lembalo, kapena kudziwitsa mfumu kumasulira kwace. 9Ndipo
mfumu Belisazara anabvutika kwambiri, ndi nkhope yace
inasandulika, ndi akuru ace anathedwa nzeru. 10Cifukwa ca mau a
mfumu ndi akuru ace mkazi wamkuru wa mfumu analowa
m'nyumba ya madyerero; mkazi wa mfumu ananena, nati, Mfumu,
mukhale ndi moyo kosatha; asakubvuteni maganizo anu, ndi
nkhope yanu isasandulike; 11pali munthu m'ufumu mwanu mwa
iye muli mzimu wa milungu yoyera; ndipo masiku a atate wanu
munapezeka mwa iye kuunika, ndi luntha, ndi nzeru, ngati nzeru
ya milungu; ndipo mfumu Nebukadinezara atate wanu, inde
mfumu atate wanu anamuika akhale mkuru wa alembi, openda,
Akasidi, ndi alauli; 12popeza m'Danieli yemweyo, amene mfumu
adamucha Belitsazara, mudapezeka mzimu wopambana, ndi
cidziwitso, ndi luntha, kumasulira maloto ndi kutanthauzira mau
ophiphiritsa, ndi kumasula mfundo. Amuitane Danieli tsono, iye
adzafotokozera kumasuliraku.

Danieli amasulira lemba lolembedwa pakhoma

13Pamenepo analowa naye Danieli kwa mfumu. Mfumu inayankha,
niti kwa Danieli, Ndiwe kodi Danieli uja wa ana a ndende a Yuda,
amene mfumu atate wanga anatenga ku Yuda? 14Ndamva za iwe
kuti muli mzimu wa milungu mwa iwe, ndi kuti mupezeka mwa iwe

kuunika, ndi luntha, ndi nzeru zopambana. 15Ndipo tsono
anabwera nao kwa ine anzeru, openda, kuti awerenge lemba ilo,
ndi kundidziwitsa kumasulira kwace; koma sanakhoza kufotokozera
kumasulira kwa cinthuci. 16Koma ndamva ine za iwe, kuti ukhoza
kutanthauzira mau, ndi kumasula mfundo; tsono ukakhoza
kuwerenga lembalo, ndi kundidziwitsa kumasulira kwace,
udzabvekedwa cibakuwa, ndi unyolo wagolidi m'khosi mwako;
nudzakhala wolamulira wacitatu m'ufumuwo. 17Pamenepo
anayankha Danieli, nati kwa mfumu, Mphatso zanu zikhale zanu,
ndi mphotho zanu mupatse wina; koma ndidzawerengera mfumu
lembalo, ndi kumdziwitsa kumasulira kwace. 18Mfumu inu,
Mulungu Wam'mwambamwamba anapatsa Nebukadinezara atate
wanu ufumuwu, ndi ukulu, ndi ulemerero, ndi cifumu; 19ndipo
cifukwa ca ukulu adampatsawo anthu onse, mitundu yonse ya
anthu, a manenedwe onse, ananjenjemera, naopa pamaso pace;
amene anafuna kuwapha anawapha; amene anafuna kuwasunga
anawasunga amoyo; amene anafuna kuwakweza anawakweza;
amene anafuna kuwatsitsa anawatsitsa. 20Koma pokwezeka mtima
wace, nulimba mzimu wace kucita modzikuza, anamtsitsa pa
mpando wa ufumu wace, namcotsera ulemerero wace; 21ndipo
anamuinga kumcotsa kwa ana a anthu, ndi mtima wace
unasandulika ngati wa nyama za kuthengo, ndi pokhala pace mpa
mbidzi, anamdyetsa udzu ngati ng'ombe, ndi thupi lace
linakhathamira ndi mame a kumwamba; mpaka anadziwa kuti
Wam'mwambamwamba alamulira m'ufumu wa anthu, nauikira ali
yense Iye afuna mwini. 22Ndipo inu mwana wace, Belisazara inu,
simunadzicepetsa m'mtima mwanu, cinkana munazidziwa izi
zonse; 23koma munadzikweza kutsutsana naye Ambuye wa
Kumwamba; ndipo anabwera nazo zotengera za nyumba yace kwa
inu; ndi inu ndi akuru anu, akazi anu ndi akazi anu ang'ono,
mwamweramo vinyo; mwalemekezanso milungu yasiliva, ndi
yagolidi, yamkuwa, yacitsulo, yamtengo, ndi yamwala, imene
siiona, kapena kumva, kapena kudziwa; ndi Mulungu amene
m'dzanja mwace muli mpweya wanu, ndi njira zanu zonse,
yemweyo simunamcitira ulemu. 24Pamenepo nsonga ya dzanja
inatumidwa kucokera pamaso pace, nililembedwa
lembali. 25Ndipolembalolembedwa ndi ili: MENE MENE TEKEL UF
ARSIN. 26Kumasulira kwace kwa mau awa ndi uku: MENE, Mulungu
anawerenga ufumu wanu, nautha. 27TEKEL, Mwayesedwa
pamiyeso, nimupezeka mwaperewera. 28PERES, ufumu wanu
wagawika, nuperekedwa kwa Amedi ndi Aperisi. 29Pamenepo
Belisazara analamulira, ndipo anabveka Danieli cibakuwa, ndi
unyolo wagolidi m'khosi mwace, nalalikira za iye kuti ndiye
wolamulira wacitatu m'ufumumo. 30Usiku womwewo Belisazara

mfumu ya Akasidi anaphedwa. 31Ndipo Dariyo Mmedi analandira ufumuwo ali wa zaka makumi asanu ndi limodzi mphambu ziwiri.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Akalonga amchulira Danieli cifukwa kwa Dariyo

1Kudamkomera Dariyo kuikira ufumuwo akalonga zana limodzi
mphambu makumi awiri akhale m'madera onse a ufumu; 2ndi
akuyang'anira iwo akulu atatu, woyamba wao ndi Danieli; kuti
akalonga awa adziwerengere kwa iwo, ndi kuti za mfumu
zisasoweke. 3Pamenepo Danieli amene anaposa akuluwa ndi
akalonga, popeza munali mzimu wopambana mwa iye, ndi mfumu
inati imuike woyang'anira ufumu wonse. 4Ndipo akuluwa ndi
akalonga anayesa kumtola cifukwa Danieli, kunena za ufumuwo;
koma sanakhoza kupeza cifukwa kapena colakwira, popeza anali
wokhulupirika; ndipo sanaona cosasamala kapena colakwa ciri
conse mwa iye. 5Pamenepo anthu awa anati, Sitidzamtola cifukwa
ciri conse Danieli amene, tikapanda kumtola ici pa cilamulo ca
Mulungu wace. 6Ndipo akuru awa ndi akalonga anasonkhana kwa
mfumu mofulumira, natero nayo, Mfumu Dariyo, mukhale ndi
moyo cikhalire. 7Akuru onse a ufumuwo, ndi akazembe ndi
akalonga, mandoda, ndi ziwanga, anapangana kukhazika lemba
lacifumu, ndi kuikapo coletsa colimba, kuti ali yense akapempha
kanthu kwa mulungu ali yense, kapena kwa munthu ali yense
masiku makumi atatu, osati kwa inu nokha, mfumu, adzaponyedwa
m'dzenje la mikango, 8Tsopano, mfumu, mukhazikitse coletsaco,
ndi kutsimikiza colembedwaco, kuti cisasinthike monga mwa
malamulo a Amedi ndi Aperisi, amene sasinthika. 9Momwemo
mfumu Dariyo anatsimikiza colembedwa ndi coletsaco. 10Ndipo
podziwa Danieli kuti adatsimikiza colembedwaco, analowa
m'nyumba mwace, m'cipinda mwace, cimene mazenera ace
anatseguka oloza ku Yerusalemu; ndipo anagwadamaondo ace
tsiku limodzi katatu, napemphera, nabvomereza pamaso pa
Mulungu wace monga umo amacitira kale lonse. 11Pamenepo
anasonkhana anthu awa, napeza Danieli alikupemphera ndi
kupembedza pamaso pa Mulungu wace. 12Ndipo anayandikira,
nanena pamaso pa mfumu za coletsaco ca mfumu, Kodi
simunatsimikiza coletsaco, kuti ali yense akapempha kanthu kwa
mulungu ali yense, kapena kwa munthu ali yense, masiku makumi
atatu, osati kwa inu nokha, mfumu, adzaponyedwa m'dzenje la
mikango? Mfumu niyankha, niti, Coona cinthuci, monga mwa
malamulo a Amedi ndi Aperisi amene sasinthika. 13Pamenepo
anayankha, nati pamaso pa mfumu, Danieli uja wa ana a ndende a
Yuda sasamalira inu, mfumu, kapena coletsa munacitsimikizaco;
koma apempha pemphero lace katatu tsiku limodzi. 14Ndipo
mfumu m'mene atamva mau awa anaipidwa kwambiri, naika
mtima wace pa Danieli kuti amlanditse, nayesetsa mpaka polowa
dzuwa kumlanditsa. 15Koma anthu awa anasonkhana kwa mfumu,

nati kwa mfumu, Dziwani, mfumu, kuti lamulo la Amedi ndi Aperisi, ndilo kuti coletsa ciri conse ndi lemba liri lonse idazikhazikira mfumu, zisasinthike.

Danieli aponyedwa m'dzenje la mikango

16Pamenepo inalamula mfumu, ndipo anadza naye Danieli, namponya m'dzenje la mikango. Ndipo mfumu inalankhula, niti kwa Danieli, Mulungu wako amene umtumikira kosalekeza, Iyeyu adzakulanditsa. 17Ndipo anatenga mwala, nauika pakamwa pa dzenje, niukomera mfumu ndi cosindikizira cace, ndi cosindikizira ca akuru ace, kuti kasasinthike kanthu ka Danieli. 18Pamenepo mfumu inamuka ku cinyumba cace, nicezera kusala usikuwo, ngakhale zoyimbitsa sanabwera nazo pamaso pace, ndi m'maso mwace munamuumira. 19Nilawira mamawa mfumu, nimuka mofulumira ku dzenje la mikango. 20Ndipo poyandikira padzenje inapfuula ndi mau acisoni mfumu, ninena, niti kwa Danieli, Danieli, mnyamata wa Mulungu wamoyo, kodi Mulungu wako, amene umtumikira kosalekeza, wakhoza kukulanditsa kwamikango? 21Pamenepo Danieli anati kwa mfumu, Mfumu, mukhale ndi moyo cikhalire. 22Mulungu wanga watuma mthenga wace, natseka pakamwa pa mikango; ndipo siinandipweteka, cifukwa anandiona wosacimwa pamaso pace, pamaso panunso, mfumu, sindinalakwa. 23Pamenepo mfumu inakondwera kwambiri, niwauza aturutse Danieli m'dzenje. Momwemo anamturutsa Danieli m'dzenje, ndi pathupi pace sipadaoneka bala, popeza anakhulupirira Mulungu wace. 24Ndipo italamulira mfumu, anabwera nao amuna aja adamneneza Danieli, nawaponya m'dzenje la mikango, iwowa, ana ao, ndi akazi ao; ndipo asanafike pansi pa dzenje mikango inawaposa mphamvu, niphwanya mafupa ao onse.

25Pamenepo mfumu Dariyo analembera kwa anthu, mitundu ya anthu, ndi a manenedwe onse okhala pa dziko lonse lapansi, Mtendere ucurukire inu. 26Ndilamulira ine kuti m'maiko onse a ufumu wanga anthu anjenjemere, naope pamaso pa Mulungu wa Danieli; pakuti Iye ndiye Mulungu wamoyo wakukhala cikhalire, ndi ufumu wace ngwosaonongeka, ndi kulamulira kwace kudzakhala mpaka cimariziro. 27Iye apulumutsa, nalanditsa, nacita zizindikilo ndi zozizwa m'mwamba ndi pa dziko lapansi, ndiye amene anapulumutsa Danieli ku mphamvu ya mikango. 28Momwemo Danieli amene anakuzikabe pokhala Dariyo mfumu, ndi pokhala mfumu Koresi wa ku Perisiya.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masomphenya a Danieli a zamoyo zinai ndi Nkhalamba ya kale lomwe

1Caka coyamba ca Belisazara mfumu ya ku Babulo Danieli anaona loto, naona masomphenya a m'mtima mwace pakama pace; ndipo analemba lotolo, nalifotokozera, mwacidule. 2Danieli ananena, nati, Ndinaona m'masomphenya anga usiku, taonani, mphepo zinai za mumlengalenga zinabuka pa nyanja yaikuru. 3Ndipo zinaturuka m'nyanja zirombo zazikuru zinai zosiyana-siyana. 4Coyamba cinanga mkango, cinali nao mapiko a ciombankhanga, ndinapenyera mpaka nthenga zace zinathothoka, nicinakwezeka kudziko, ndi kuimitsidwa ndi mapazi awiri ngati munthu, nicinapatsidwa mtima wa munthu. 5Ndipo taonani, cirombo cina caciwiri cikunga cimbalangondo cinatundumuka mbali imodzi; ndi m'kamwa mwace munali nthiti zitatu pakati pa mano ace; ndipo anatero naco, Nyamuka, lusira nyama zambiri. 6Pambuyo pace ndinapenya ndi kuona cina ngati nyalugwe, cinali nao mapiko anai a nkhuku pamsana pace, ciromboco cinali nayonso mitu inai, nicinapatsidwa ulamuliro. 7Pambuyo pace ndinaona m'masomphenya a usiku, ndi kuona cirombo cacinai, coopsa ndi cocititsa mantha, ndi camphamvu coposa, cinali nao mano akuru acitsulo, cinalusa ndi kuphwanya ndi kupondereza cotsala ndi mapazi ace; cinasiyana ndi zirombo zonse zidacitsogolera; ndipo cinali ndi nyanga khumi. 8Ndinali kulingirira za nyangazi, taonani, pakati pa izo panaphuka nyanga yina, ndiyo yaing'ono; patsogolo pace zitatu za nyanga zoyambazi zinazulidwa ndi mizu yomwe; ndipo taonani, m'nyanga m'menemo munali maso ngati maso a munthu, ndi pakamwa palikunena zazikuru. 9Ndinapenyerera mpaka anaikapo mipando yacifumu, nikhalapo Nkhalamba ya kale lomwe, zobvala zace zinali za mbu ngati cipale cofewa, ndi tsitsi la pa mutu pace ngati ubweya woyera, mpando wacifumu unali malawi amoto, ndi njinga zace moto woyaka. 10Mtsinje wamoto unayenda woturuka pamaso pace, zikwi zikwi anamtumikira, ndi unyinji wosawerengeka unaima pamaso pace, woweruza mlandu anakhalapo, ndi mabuku anatsegulidwa. 11Pamenepo ndinapenyera cifukwa ca phokoso la mau akuru idanena nyangayi; ndinapenyera mpaka adacipha ciromboci, ndi kuononga mtembo wace, ndi kuupereka utenthedwe ndi moto. 12Ndipo zirombo zotsalazo anazicotsera ulamuliro wao, koma anatalikitsa moyo wao, ukhalenso nyengo ndi nthawi. 13Ndinaona m'masomphenya a usiku, taonani, anadza ndi mitambo ya kumwamba wina ngati mwana wa munthu, nafika kwa Nkhalamba ya kale lomwe; ndipo anamyandikizitsa pamaso pace. 14Ndipo anampatsa ulamuliro, ndi ulemerero, ndi ufumu, kuti anthu onse, ndi mitundu yonse ya anthu, ndi a manenedwe onse, amtumikire; ulamuliro wace ndi ulamuliro wosatha wosapitirira, ndi ufumu wace sudzaonongeka.

Kumasulira kwa masomphenyawo

15Koma ine Danieli, mzimu wanga unalaswa m'kati mwa thupi langa, ndi masomphenya a m'mtima mwanga anandibvuta. 16Ndinayandikira kwa wina wa iwo akuimako ndi kumfunsa za coonadi za ici conse. Ndipo ananena nane, nandidziwitsa kumasulira kwace kwa zinthuzi: 17Zirombo zazikuru izi zinai ndizo mafumu anai amene adzauka pa dziko lapansi. 18Koma opatulika la Wam'mwambamwamba adzalandira ufumuwo, ndi kukhala nao ufumu kosatha, ku nthawi zomka muyaya. 19Pamenepo ndinafuna kudziwa coonadi ca cirombo cacinai cija cidasiyana nazo zonsezi, coopsa copambana, mano ace acitsulo, ndi makadabo ace amkuwa, cimene cidalusa, ndi kuphwanya, ndi kupondereza zotsala ndi mapazi ace; 20ndi za nyanga khumi zinali pamutu pace, ndi nyanga yina Idaphukayi, imene zidagwa zitatu patsogolo pace; nyangayo idali ndi maso ndi pakamwa pakunena zazikuru, imene

maonekedwe ace anaposa zinzace. 21Ndinapenya, ndipo nyanga yomweyi
inacita nkhondo ndi opatulikawo, niwalaka, mpaka inadza Nkhalamba ya kale
lomwe; 22ndi mlandu unakomera opatulika a Wam'mwambamwamba, nifika
nthawi yakuti ufumu unali wao wa opatulikawo. 23Anatero, cirombo cacinai
ndico ufumu wacinai pa dziko lapansi, umene udzasiyana nao maufumu onse,
nudzalusira dziko lonse lapansi, nudzalipondereza ndi kuliphwanya. 24Kunena
za nyanga khumi, m'ufumu uwu adzauka mafumu khumi, ndi pambuyo pao
idzauka yina; iyo idzasiyana ndi oyamba aja, nidzacepetsa mafumu
atatu. 25Nidzanena mau akutsutsana ndi Wam'mwambainwamba,
nidzalemetsa opatulika a Wam'mwambamwamba, nidzayesa kusintha
nthawizo ndi cilamulo; ndipo adzaperekedwa m'dzanja lace mpaka nthawi
imodzi, ndi nthawi zina, ndi nthawi yanusu. 26Koma woweruza mlandu
adzakhalako, ndipo adzacotsa ulamuliro wace, kuutha ndi kuuononga kufikira
cimariziro. 27Ndipo ufumu, ndi ulamuliro, ndi ukulu wa maufumu, pansi pa
thambo lonse, zidzapatsidwa kwa anthu a opatulika a
Wam'mwambamwamba; ufumu wace ndiwo ufumu wosatha, ndi maiko onse
adzamtumikira ndi kummvera. 28Kutha kwace kwa cinthuci nkuno. Ine Danieli,
maganizo anga anandibvuta kwambiri, ndi nkhope yanga inasandulika; koma
ndinasunga cinthuci m'mtima mwanga.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masomphenya a nkhosa yamphongo ndi tonde

1Caka cacitatu ca Belisazara mfumu masomphenya anandionekera
kwa ine Danieli, atatha kundionekera oyamba aja. 2Ndipo ndinaona
m'masomphenya; tsono kunali, pakuwaona ine ndinali m'Susani,
m'nyumba ya mfumu, ndiwo m'dziko la Elamu; ndinaona
m'masomphenya kuti ndinali kumtsinje Ulai. 3Ndipo ndinakweza
maso anga ndi kupenya; taonani, panaima pamtsinje nkhosa
yamphongo yokhala nazo nyanga ziwiri, ndi nyanga ziwirizo zinali
za msinkhu wautali, koma imodzi inaposa inzace; yoposayo
inaphuka m'mbuyo. 4Ndinaona nkhosa yamphongo irikugunda
kumadzulo, ndi kumpoto, ndi kumwela; ndipo panalibe zamoyo
zokhoza kuima pamaso pace; panalibenso wakulanditsa m'dzanja
lace; koma inacita monga mwa cifuniro cace, nidzikulitsa. 5Ndipo
polingirfrapo ine, taonani, wadza tonde wocokera kumadzulo, pa
nkhope ya dziko lonse lapansi, wosakhudza nthaka; ndi mbuziyo
inali ndi nyanga yooneka bwino pakati pa maso ace. 6Ndipo
anadzera nkhosa yamphongoyo yokhala ndi nyanga ziwiri, imene
ndidaiona irikuima kumtsinje, naithamangira ndi mphamvu yace
yaukali. 7Ndipo ndinamuona wayandikira pafupi pa nkhosa
yamphongo, nawawidwa mtima nayo, naigunda nkhosa
yamphongo, natyola nyanga zace ziwiri; ndipo mphongoyo inalibe
mphamvu yakuima pamaso pace, koma anaigwetsa pansi,
naipondereza; ndipo panalibe wakupulumutsa mphongoyo
m'dzanja lace. 8Ndipo tondeyo anadzikulitsa kwakukuru, koma
atakhala wamphamvu, nyanga yace yaikuru inatyoka; ndi m'malo
mwace munaphuka nyanga zinai zooneka bwino, zoloza ku
mphepo zinai za mlengalenga. 9Ndipo mu imodzi ra izi munaphuka
nyanga yaing'ono, imene inakula kwakukuru ndithu, kuloza
kumwela, ndi kum'mawa, ndi ku dziko lokometsetsa. 10Nikula,
kufikira khamu la kuthambo; ndi zina za khamulo ndi za nyenyezi
inazigwetsa pansi, niziponderezа. 11Inde inadzikulitsa kufikira kwa
kalonga wa khamulo, nimcotsera nsembe yopsereza yacikhalire;
ndi pokhala malo ace opatulika panagwetsedwa. 12Ndipo khamulo
linaperekedwa kwa iyo, pamodzi ndi nsembe yopsereza yacikhalire
mwa kulakwa kwace, nigwetsa pansi coonadi, nicita cifuniro cace,
nikuzika. 13Pamenepo ndinamva wina woyera, alikunena; ndi wina
woyera anati kwa iye uja wanenayo, Masomphenya a nsembe
yopsereza yacikhalire, ndi colakwa cakupululutsa ca kupereka
malo opatulika ndi khamulo ziponderezedwe, adzakhala mpaka
liti? 14Nati kwa ine, Mpaka masiku zikwi ziwiri mphambu mazana
atatu usana ndi usiku; pamenepo malo opatulika adzayesedwa
olungama.

15Ndipo kunali, nditaona masomphenyawo, ine Danieli ndinafuna
kuwazindikira; ndipo taonani, panaima popenyana ndi ine ngati
maonekedwe a munthu. 16Ndipo ndinamva mau a munthu pakati
pa magombe a Ulai, naitana, nati, Gabrieli, zindikiritsa munthuyu
masomphenyawo. 17Nayandikira iye poima inepo; atadza iye tsono
ndinacita mantha, ndinagwa nkhope pansi; koma anati kwa ine,
Zindikira, wobadwa ndi munthu iwe, pakuti masomphenyawo
anena za nthawi ya cimariziro. 18Ndipo m'mene analikulankhula
ndi ine ndinagwidwa ndi tulo tatikuru, nkhope yanga pansi; koma
anandikhudza, nandiimiritsa pokhala inepo, 19Ndipo anati, Taona,
ndidzakudziwitsa cimene cidzacitika pa citsiriziro ca mkwiyowo;
pakuti pa nthawi yoikika mpakutha pace, 20Nkhosa yamphongo
waiona ya nyanga ziwiri ndizo mafumu a Mediya ndi Perisiya. 21Ndi
tonde wamanyenje ndiye mfumu ya Helene, ndi nyanga yaikuru iri
pakati pa maso ace ndiyo mfumu yoyamba. 22Ndi kuti zinaphuka
zinai m'malo mwace mwa iyo itatyoka, adzauka maufumu anai
ocokera mu mtunduwu wa anthu, koma osakhala nayo mphamvu
ya uja. 23Ndipo potsiriza pace pa ufumu wao, atakwanira olakwa,
idzauka mfumu ya nkhope yaukali yakuzindikira zinsinsi. 24Ndi
mphamvu yace idzakhala yaikuru, koma si mphamvu yace yace ai,
nidzaononga modabwiza, nidzakuzika, ndi kucita, ndi kuononga
amphamvuwo, ndi anthu opatulikawo. 25Ndipo mwa kucenjera
kwace adzapindulitsa cinyengo m'dzanja mwace, nadzadzikuza
m'mtima mwace; ndipo posatekeseka anthu, adzaononga ambiri;
adzaukiranso kalonga wa akalonga, koma adzatyoledwa popanda
dzanja. 26Ndipo masomphenya a madzulo ndi mamawa
adanenawo ndi oona; koma iwe ubise masomphenyawo, popeza
adzacitika atapita masiku ambiri. 27Ndipo ine Danieli ndinakomoka
ndi kudwala masiku ena; pamenepo ndinauka ndi kucita nchito ya
mfumu; ndipo ndinadabwa nao masomphenyawo, koma panalibe
wakuwazindikiritsa.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Pemphero la Danieli

1Caka coyamba ca Dariyo mwana wa Ahaswero, wa mbeu ya
Amedi, amene anamlonga mfumu ya Akasidi; 2caka coyamba ca
ufumu wace, ine Danieli ndinazindikira mwa mabuku kuti
ciwerengo cace ca zaka, cimene mau a Yehova anadzera naco kwa
Yeremiya mneneri, kunena za makwaniridwe a mapasuko a
Yerusalemu, ndizo zaka makumi asanu ndi awiri. 3Ndipo ndinaika
nkhope yanga kwa Ambuye Mulungu, kumfunsa Iye m'pemphero,
ndi mapembedzero, ndi kusala, ndi ziguduli, ndi mapulusa. 4Ndipo
ndinapemphera kwa Yehova Mulungu wanga ndi kubvomereza, ndi
kuti, Ambuye Mulungu wamkuru ndi woopsa, wakuwasungira
pangano ndi cifundo iwo akukukondani, ndi kusunga malamulo
anu, 5tacimwa, tacita mphulupulu, tacita zoipa, tapanduka,
kupambuka ndi kusiya maneno anu ndi maweruzo
anu; 6sitinamvera atumiki anu aneneri, amene ananena m'dzina
lanu kwa mafumu athu, akalonga athu, makolo athu, ndi anthu
onse a m'dziko. 7Ambuye, cilungamo nca Inu, koma kwa ife
manyazi a nkhope yathu, monga lero lino; kwa anthu a Yuda, ndi
kwa okhala m'Yerusalemu, ndi kwa Aisrayeli onse okhala pafupi ndi
okhala kutali, ku maiko onse kumene mudawaingira, cifukwa ca
kulakwa kwao anakulakwirani nako. 8Ambuye, kwa ife kuli manyazi
a nkhope yathu, kwa mafumu athu, kwa akalonga athu, ndi kwa
makolo athu; pakuti takucimwirani. 9Ambuye Mulungu wathu ndiye
wacifundo, ndi wokhululukira; pakuti tampandukira
Iye; 10sitinamvera mau a Yehova Mulungu wathu, kuyenda
m'malamulo ace anatiikirawo pamaso pathu, mwa atumiki ace
aneneri. 11Inde Israyeli yense walakwira cilamulo canu, ndi
kupambuka, kuti asamvere mau anu; cifukwa cace temberero
lathiridwa pa ife, ndi Ilumbiro lolembedwa m'cilamulo ca Mose
mtumiki wa Mulungu; pakuti tamcimwira. 12Ndipo anakwaniritsa
mau ace adanenawo, kutitsutsa ife ndi oweruza athu otiweruza,
ndi kutitengera coipa cacikuru; pakuti pansi pa thambo lonse
sipanacitika monga umo panacitikira Yerusalemu. 13Monga
mulembedwa m'cilamulo ca Mose coipa ici conse catidzera; koma
sitinapepeza Yehova Mulungu wathu, ndi kubwera kuleka
mphulupulu zathu, ndi kucita mwanzeru m'coonadi
canu. 14Cifukwa cace Yehova wakhala maso pa coipaco, ndi
kutifikitsira ico; pakuti Yehova Mulungu wathu ali wolungama mu
nchito zace zonse azicita; ndipo sitinamvera mau ace. 15Ndipo
tsopano, Ambuye Mulungu wathu, amene munaturutsa anthu anu
m'dziko la Aigupto ndi dzanja lamphamvu, ndi kudzitengera mbiri
monga lero lino, tacimwa, tacita coipa. 16Ambuye, monga mwa
cilungamo canu conse, mkwiyo wanu ndi ukali wanu

zitembenuketu, zicoke ku mudzi wanu Yerusalemu, phiri lanu lopatulika; pakuti mwa zocimwa zathu, ndi mphulupulu za makolo athu, Yerusalemu ndi anthu anu asanduka cotonza ca onse otizungulira. 17Ndipo tsopano, Mulungu wathu, mumvere pemphero la mtumiki wanu, ndi mapembedzero ace, nimuwalitse nkhope yanu pa malo anu opatulika amene ali opasuka, cifukwa ca Ambuye, 18Mulungu wanga, cherani khutu, nimumvere, tsegulani maso anu, nimupenye zopasuka zathu, ndi mudzi udachedwawo dzina lanu; pakuti sititula mapembedzero athu pamaso panu, cifukwa ca nchito zathu zolungama, koma cifukwa ca zifundo zanu zocuruka. 19Ambu ye, imvani; Ambuye, khululukirani; Ambuye, mverani nimucite; musacedwa, cifukwa ca inu nokha, Mulungu wanga; pakuti mudzi wanu ndi anthu anu anachedwa dzina lanu.

Masabata makumi asanu ndi awiriwo, ndi Wodzozedwayo

20Ndipo pakunena ine, ndi kupemphera, ndi kubvomereza cimo langa, ndi cimo la anthu amtundu wanga Israyeli, ndi kutula cipembedzero canga pamaso pa Yehova Mulungu wanga, cifukwa ca phiri lopatulika la Mulungu wanga; 21inde pakunena ine m'kupemphera, munthu uja Gabrieli, amene ndidamuona m'masomphenya poyamba paja, anauluka mwaliwiro nandikhudza ngati nthawi yakupereka nsembe ya madzulo. 22Ndipo anandilangiza ine, ndi kulankhula nane, nati, Danieli iwe, ndaturuka tsopano ine kukuzindikiritsa mwaluntha. 23Pakuyamba iwe mapembedzero ako, linaturuka lamulo; ndipo ndadza ine kukufotokozera; pakuti ukondedwa kwambiri; zindikira tsono mau awa, nulingirire masomphenyawo. 24Masabata makumi asanu ndi awiri alamulidwira anthu amtundu wako ndi mudzi wako wopatulika, kumariza colakwaco, ndi kutsiriza macimo, ndi kutetezera mphulupulu, ndi kufikitsa cilungamo cosalekeza, ndi kukhomera cizindikilo masomphenya ndi zonenera, ndi kudzoza malo opatulikitsa. 25Dziwa tsono, nuzindikire, kuti kuyambira kuturuka lamulo lakukonzanso, ndi kummanga Yerusalemu, kufikira wodzozedwayo, ndiye kalonga, kudzakhala masabata asanu ndi awiri; ndi masabata makumi asanu ndi limodzi mphambu awiri makwalala ndi chemba zidzamangidwanso, koma mu nthawi za mabvuto. 26Ndipo atapita masabata makumi asanu ndi limodzi mphambu awiri wodzozedwayo adzalikhidwa, nadzakhala wopanda kanthu; ndi anthu a kalonga wakudzayo adzaononga mudzi ndi malo opatulika; ndi kutsiriza kwace kudzakhala kwa cigumula, ndi kufikira cimariziro kudzakhala nkhondo; cipasuko calembedweratu. 27Ndipo iye adzapangana cipangano colimba ndi ambiri sabata limodzi; ndi pakati pa sabata adzaleketsa nsembe yophera ndi nsembe yaufa; ndi pa phiko la zonyansa padzafika

wina wakupasula, kufikira cimariziro colembedweratu, mkwiyo udzatsanulidwa pa wopasulayo.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Danieli aona masomphenya oopsa, mngelo amlimbikitsa

1Caka cacitatu ca Koresi mfumu ya Perisiya, cinabvumbulutsidwa
cinthu kwa Danieli, amene anamucha Belitsazara; ndipo cinthuco
ncoona, ndico nkhondo yaikuru; ndipo anazindikira cinthuco,
nadziwa masomphenyawo. 2Masiku aja ine Danieli ndinali kulira
masabata atatu amphumphu, 3Cakudya cofunika osacidya ine,
nyama kapena vinyo zosapita pakamwa panga, osadzola ine
konse, mpaka anakwaniridwa masabata atatu amphumphu, 4Ndipo
tsiku la makumi awiri mphambu anai la mwezi woyamba, pokhala
ine m'mphepete mwa mtsinje waukuru, ndiwo
Hidikeli, 5ndinakweza maso anga, ndinapenya ndi kuona munthu
wobvala bafuta, womanga m'cuuno ndi golidi woona wa ku
Ufazi; 6thupi lace lomwe linanga berulo, ndi nkhope yace ngati
maonekedwe a mphezi, ndi maso ace ngati nyali zamoto, ndi
manja ace ndi mapazi ace akunga mkuwa wonyezimira, ndi
kumveka kwa mau ace kunanga phokoso la aunyinji. 7Ndipo ine
Danieli ndekha ndinaona masomphenyawo; pakuti anthu anali
nane sanaona masomphenyawo; koma kunawagwera
kunjenjemera kwakukuru, nathawa kubisala. 8Momwemo
ndinatsala ndekha, ndipo ndinaona masomphenya akuruwa, koma
wosakhala ndi mphamvu ine; pakuti kukoma kwanga
kunasandulika cibvundi mwa ine, wosakhalanso ndi mphamvu
ine. 9Ndipo ndinamva kunena kwa mau ace, ndipo pamene
ndinamva kunena kwa mau ace ndinagwidwa ndi tulo tatikuru
pankhope panga, nkhope yanga pansi. 10Ndipo taonani,
linandikhudza dzanja ndi kundikhalitsa ndi maondo anga, ndi
zikhato za manja anga. 11Nati kwa ine, Danieli, munthu
wokondedwatu iwe, tazindikira mau ndirikunena ndi iwe, nukhale
ciriri; pakuti ndatumidwa kwa iwe tsopano. Ndipo pamene adanena
mau awa kwa ine ndinaimirira ndi kunjenjemera. 12Pamenepo anati
kwa ine, Usaope Danieli; pakuti kuyambira tsiku loyamba lija
unaika mtima wako kuzindikira ndi kudzicepetsa pamaso pa
Mulungu wako, mau ako anamveka; ndipo ndadzera mau
ako, 13Koma kalonga wa ufumu wa Perisiya ananditsekerezera njira
masiku makumi awiri ndi limodzi; ndipo taonani, Mikaeli, wina wa
akalonga omveka, anadza kundithandiza; ndipo ndinakhala
komweko ndi mafumu a Perisiya. 14Ndadzera tsono kukuzindikiritsa
codzagwera anthu a mtundu wako masiku otsiriza; pakuti
masomphenyawo ndiwo a masiku a m'tsogolo. 15Ndipo atanena
ndi ine monga mwa mau awa, ndinaweramitsa nkhope yanga
pansi ndi kukhala du. 16Ndipo taonani, wina wakunga ana a anthu
anakhudza milomo yanga; pamenepo ndinatsegula pakamwa
panga ndi kunena naye woima popenyana nane, Mbuye wanga,

cifukwa ca masomphenyawo zowawa zanga zandibwerera, ndipo ndiribenso mphamvu. 17Pakuti mnyamata wa mbuye wanga inu akhoza bwanji kulankhula ndi mbuye wanga inu? pakuti ine tsopano apa mulibenso mphamvu mwa ine, osanditsaliranso mpweya.

Nkhondo ya pakati pa Perisiya ndi Helene

18Pamenepo anandikhudzanso wina, maonekedwe ace ngati munthu, nandilimbikitsa ine. 19Nati, Munthu wokondedwatu iwe, Usaope, mtendere ukhale nawe; limbika, etu limbika. Ndipo pamene ananena ndi ine ndinalimbikitsidwa, ndinati, Anene mbuye wanga; pakuti mwandilimbikitsa. 20Pamenepo anati, Kodi udziwa cifukwa coti ndakudzera? ndipo tsopano ndibwerera kulimbana ndi kalonga wa Perisiya; ndipo pomuka ine, taonani, adzadza kalonga wa Helene. 21Koma ndidzakufotokozera colembedwa pa lemba la coonadi; ndipo palibe wina wakudzilimbikitsa pamodzi ndi ine, kutsutsana ndi aja, koma Mikaeli kalonga wanu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

1Ndipo ine, caka coyamba ca Dariyo Mmedi, ndinauka kumlimbikitsa ndi
kumkhazikitsa.
2Ndipo tsopano ndikufotokozera coonadi. Taona, adzaukanso mafumu atatu
m'Perisiya, ndi yacinai idzakhala yoletnera ndithu yoposa onsewo; ndipo
itadzilimbitsa yokha mwa kulemera kwace idzawautsa onse alimbane nao
ufumu wa Helene. 3Ndipo idzauka mfumu yamphamvu, nidzacita ufumu ndi
ulamuliro waukuru, nidzacita monga mwa cifuniro cace. 4Ndipo pakuuka iye
ufumu wace udzatyoledwa, nudzagawikira ku mphepo zinai za mlengalenga;
koma sadzaulandira a mbumba yace akudza m'mbuyo, kapena monga mwa
ulamuliro wace anacita ufumu nao; pakuti ufumu wace udzazulidwa, ukhale
wa ena, si wa aja ai.
Nkhondo ya pakati pa mfumu ya kumpoto ndi ya kumwera
5Ndipo mfumu ya kumwela, ndiye wina wa akalonga ace, idzamposa
mphamvu, nidzakhala nao ulamuliro; ulamuliro wace ndi ulamuliro
waukuru. 6Ndipo pakutha zaka adzaphatikizana iwo; ndi mwana wamkazi wa
mfumu ya kumwela adzafika kwa mfumu ya kumpoto, kupangana naye
zoyenera koma mkaziyo sadzaisunga mphamvu ya dzanja lace; ngakhale
mwamunayo sadzaimika, ngakhale dzanja lace; koma mkaziyo
adzaperekedwa, pamodzi ndi iwo adadza naye, ndi iye amene anambala, ndi
iye amene anamlimbitsa nthawi zija. 7Koma apo pophukira mizu yace adzauka
wina m'malo mwace, ndiye adzafika kulimbana nalo khamu la nkhondo,
nadzalowa m'linga la mfumu ya kumpoto, nadzacita molimbana nao,
nadzawalaka; 8ndi milungu yao yomwe, pamodzi ndi akalonga ao, ndi
zipangizo zao zofunika za siliva ndi golidi adzazitenga kumka nazo ndende ku
Aigupto; ndi zaka zace zidzaposa za mfumu ya kumpoto. 9Ndipo adzalowa
m'ufumu wa mfumu ya kumwela, koma adzabwera m'dziko lace lace. 10Ndi
ana ace adzacita nkhondo, nadzamemeza makamu a nkhondo akuru ocuruka,
amene adzalowa, nadzasefukira, nadzapita; ndipo adzabwerera, nadzacita
nkhondo mpaka linga lace. 11Ndi mfumu ya kumwela adzawawidwa mtima,
nadzaturuka kulimbana naye, ndiye mfumu ya kumpoto imene idzaonetsa
unyinji waukuru; koma unyinjiwo udzaperekedwa m'dzanja lace. 12Ndipo
ataucotsa unyinjiwo udzakwezeka mtima wace; ndipo adzagwetsa zikwi
makumi makumi, koma sadzalakika. 13Ndi mfumu ya kumpoto idzabwera,
nidzaimika unyinji wa kuposa oyamba aja; nidzafika pa cimariziro ca nthawi,
ca zaka, ndi khamu lalikuru la nkhondo ndi cuma cambiri. 14Ndipo nthawi zija
ambiri adzaukira mfumu ya kumwela, ndi aciwawa mwa anthu a mtundu wako
adzadzikuza kukhazikitsa masomphenyawo, koma adzagwa iwo. 15Ndi mfumu
ya kumpoto idzadza, nidzaunda mtumbira, nidzalanda midzi yamalinga; ndi
ankhondo a kumwela sadzalimbika, ngakhale anthu ace osankhika; inde
sipadzakhala mphamvu yakulimbika. 16Koma iye amene amdzera kulimbana
naye adzacita cifuniro cace ca iye mwini; palibe wakulimbika pamaso pace;
ndipo adzaima m'dziko lokometsetsalo, ndi m'dzanja mwace mudzakhala
cionongeko. 17Ndipo adzalimbitsa nkhope yace, kudza ndi mphamvu ya
ufumu wace wonse, ndi oongoka mtima pamodzi naye; ndipo adzacita cifuniro
cace, nadzampatsa mwana wamkazi wa akazi kumuipitsa; koma mkaziyo
sadzalimbika, kapena kubvomerezana naye. 18Pambuyo pace
adzatembenuzira nkhope yace kuzisumbu, nadzalanda zambiri; koma kalonga
wina adzaleketsa kunyoza kwace adanyoza nako; inde adzambwezera yekha
kunyoza kwace. 19Pamenepo adzatembenuzira nkhope yace ku malinga a
dziko lace lace; koma adzakhumudwa, nadzagwa osapezedwanso. 20Ndipo
m'malo mwace adzauka wina wakupititsa wamsonkho pa ulemerero wa

ufumuwo; koma atatha masiku owerengeka adzatyoledwa iye, si mwamkwiyo, kapena kunkhondo ai. 21Ndi m'malo mwace adzauka munthu woluluka, amene anthu sanampatsa ulemu wa ufumu, koma adzafika kacetecete, nadzalanda ufumu ndi mau osyasyalika. 22Ndipo mwa mayendedwe ace a cigumula adzakokololedwa pamaso pace, nadzatyoledwa, ngakhale kalonga yemwe wa cipangano. 23Ndipo atapangana naye adzacita monyenga; pakuti adzakwera, nadzasanduka wamphamvu ndi anthu owerengeka. 24Adzafika kacetecete ku minda yokometsetsa ya derali, nadzacita cosacita atate ace, kapena makolo ace; adzawawazira zofunkha, ndi zankhondo, ndi cuma, nadzalingiririra malinga ziwembu zace; adzatero nthawi. 25Nadzautsa mphamvu yace ndi mtima wace ayambane ndi mfumu ya kumwela ndi khamu lalikuru la nkhondo; ndi mfumu ya kumwela ndi khamu lalikuru ndi lamphamvu ndithu; koma sadzaimika, popeza adzamlingiririra ziwembu. 26Inde iwo akudyako cakudya cace adzamuononga; ndi ankhondo ace adzasefukira, nadzagwaambiri ophedwa. 27Ndipo mafumu awa onse awiri mitima yao idzakumbuka kucita zoipa, nadzanena bodza ali pa gome limodzi; koma osapindula nalo; pakuti kutha kwace kudzakhala pa nthawi yoikika. 28Ndipo adzabwerera ku dziko lace ndi cuma cambiri; ndi mtima wace udzatsutsana ndi cipangano copatulika, nadzacita cifuniro cace, ndi kubwerera ku dziko lace. 29Pa nthawi yoikika adzabwera, nadzalowa kumwela; koma sikudzakhala monga nthawi yoyamba ija, kapena yotsirizayi. 30Pakuti zombo za ku Kitimu zidzafika kuyambana naye; cifukwa cace adzatenga nkhawa, nadzabwerera, nadzaipidwa mtima ndi cipangano copatulika, nadzacita cifuniro cace; adzabweranso, nadzasamalira otaya cipangano copatulika. 31Ndipo ankhondo adzamuimirira, nadzadetsa malo opatulika ndi linga lace; nadzacotsa nsembe yosalekezayo, nadzaimitsa conyansa copululutsaco. 32Ndipo akucitira coipa cipanganoco iye adzawaipsa, ndi kuwasyasyalika; koma anthu akudziwa Mulungu wao adzalimbika mtima, nadzacita mwamphamvu. 33Ndipo aphunzitsi a anthu adzalangiza ambiri, koma adzagwa ndi lupanga, ndi lawi lamoto, ndi undende, ndi kufunkhidwa masiku ambiri. 34Ndipo pakugwa iwo adzathandizidwa ndi thandizo laling'ono; koma ambiri adzaphatikizana nao ndi mau osyasyalika. 35Nadzagwa aphunzitsi ena kuwayesa ndi moto, ndi kuwatsutsa, ndi kuwayeretsa, mpaka nthawi ya citsiriziro; pakuti kukaliko kufikira nthawi yoikika. 36Ndipo mfumu idzacita monga mwa cifuniro cace, nidzadzikweza, ndi kudzikuza koposa milungu iri yonse nidzanena zodabwiza pa Mulungu wa milungu, nidzapindula, mpaka udzacitidwa ukaliwo; pakuti cotsimikizika m'mtimaco cidzacitika. 37Ndipo sidzasamalira milungu ya makolo ace, kapena coikhumba akazi, kapena kusamalira milungu iri yonse; pakuti idzadzikuza koposa onse. 38Koma kumalo kwace idzacitira ulemu mulungu wa malinga; ndi mulungu amene makolo ace sanaudziwa, adzaulemekeza ndi golidi, ndi siliva, ndi miyala ya mtengo wace, ndi zinthu zofunika. 39Ndipo adzacita molimbana ndi malinga olimba koposa, pomthandiza mulungu wacilendo; ali yense wombvomereza adzamcurukitsira ulemu, nadzawacititsa ufumu pa ambiri, nadzagawa dziko mwa mtengo wace. 40Ndipo nthawi yotsiriza mfumu ya kumwela idzalimbana naye, ndi mfumu ya kumpoto idzamdzera ngati kabvumvulu, ndi magareta, ndi apakavalo, ndi zombo zambiri; nadzalowa m'maiko, nadzasefukira ndi kupitirira. 41Adzalowanso m'dziko lokometsetsalo ndi maiko ambiri adzapasuka; koma opulumuka dzanja lace ndi awa: Edomu, ndi Moabu, ndi oyamba a ana a Amoni. 42Adzatambalitsiranso dzanja lace kumaiko; dziko la Aigupto lomwe silidzapulumuka. 43Ndipo adzacita mwamphamvu ndi cuma ca golidi, ndi siliva, ndi zinthu zofunika zonse za

Aigupto; Alubi ndi Akusi adzatsata mapazi ace. 44Koma mbiri yocokera
kum'mawa ndi kumpoto idzambvuta; nadzaturuka iye ndi ukali waukuru kupha
ndi kuononga konse ambiri. 45Ndipo adzamanga mahema a nyumba yacifumu
yace pakati pa nyanja yamcere ndi phiri lopatulika lofunika; koma adzafikira
cimariziro cace wopanda wina wakumthandiza.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Nthawi ya cimariziro, mau otsekedwa

1Ndipo nthawi yomweyi adzauka Mikaeli kalonga wamkuru
wakutumikira ana a anthu amtundu wako; ndipo padzakhala
nthawi ya masautso, siinakhala yotere kuyambira mtundu wa
anthu kufikira nthawi yomwe ija; ndipo nthawi, yomweyo anthu
ako adzapulumutsidwa, yense amene ampeza wolembedwa
m'buku. 2Ndipo ambiri, a iwo ogona m'pfumbi lapansi adzauka,
ena kumka ku moyo wosatha, ndi ena ku manyazi ndi mnyozo
wosatha. 3Ndipo aphunzitsi adzawala ngati kunyezimira kwa
thambo; ndi iwo otembenuza ambiri atsate cilungamo ngati
nyenyezi ku nthawi za nthawi. 4Koma iwe Danieli, tsekera mau
awa, nukomere cizindikilo buku, mpaka nthawi ya cimariziro;
ambiri adzathamanga cauko ndi cauko, ndi cidziwitso cidzacuruka.
5Pamenepo ine Danieli ndinapenya, ndipo taonani, anaimapo awiri
ena, wina m'mphepete mwa mtsinje tsidya lino, ndi mnzace
m'mphepete mwa mtsinje tsidya lija. 6Ndipo wina anati kwa
munthu wobvala bafuta, wokhala pamwamba pa madzi a
mumtsinje, Cimariziro ca zodabwiza izi cidzafika liti? 7Ndipo
ndinamva munthuyo wobvala bafuta wokhala pamwamba pa
madzi a mumtsinje, nakweza dzanja lace lamanja ndi lamanzere
kumwamba, nalumbira pali Iye wokhala ndi moyo kosatha, kuti
zidzacitika nthawi, ndi nthawi zina, ndi nusu; ndipo atatha
kumwaza mphamvu ya anthu opatulikawo zidzatha izi
zonse. 8Ndinacimva ici, koma osacizindikira; pamenepo ndinati
Mbuye wanga, citsiriziro ca izi nciani? 9Ndipo anati, Pita Danieli;
pakuti mauwo atsekedwa, nakomeredwa cizindikilo mpaka nthawi
ya citsiriziro. 10Ambiri adzadzitsuka ndi kudziyeretsa,
nadzayesedwa ndi moto; koma oipa adzacita moipa; ndipo palibe
mmodzi wa oipa adzazindikira; koma aphunzitsi ndiwo
adzazindikira. 11Ndipo kuyambira nthawi yoti idzacotsedwa
nsembe yacikhalire, nicidzaimika conyansa cakupululutsa,
adzakhalanso masiku cikwi cimodzi mphambu mazana awiri kudza
makumi asanu ndi anai. 12Wodala iye amene ayembekeza, nafikira
ku masiku cikwi cimodzi mphambu mazana atatu kudza makumi
atatu ndi asanu. 13Koma iwe, muka mpaka cimariziro; pakuti
udzapumula, nudzaima m'gawo lako masiku otsiriza.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Hosea

Hoseya 1

Hoseya akwatira mkazi woipa kufanizira zoipa za Israyeli

1MAU a Yehova amene anadza kwa Hoseya mwana wa Beeri
masiku a Uziya, Yotamu, Ahazi, ndi Hezekiya, mafumu a Yuda, ndi
masiku a Yerobiamu mwana wa Yoasi mfumu ya Israyeli.
2Ciyambi ca kunena kwa Yehova mwa Hoseya, Ndipo Yehova anati
kwa Hoseya, Muka, udzitengere mkazi wacigololo ndi ana
acigololo; pakuti dziko latsata cigololo cokha cokha kuleka kutsata
Yehova. 3Ndipo anamuka natenga Gomeri mwana wamkazi wa
Diblaimu; iye naima, nambalira mwana wamwamuna. 4Ndipo
Yehova anati kwa iye, Umuche dzina lace Yezreeli; pakuti katsala
kanthawi, ndipo ndidzabwezera cilango mwazi wa Yezreeli pa
nyumba ya Yehu, ndi kuleketsa ufumu wa nyumba ya
Israyeli. 5Ndipo kudzacitika tsiku lomwelo, ndidzatyola uta wa
Israyeli m'cigwa ca Yezreeli. 6Ndipo anaimanso, nabala mwana
wamkazi. Ndipo Yehova anati kwa iye, Umuche dzina lace
Wosacitidwacifundo; pakuti sindidzacitiranso cifundo nyumba ya
Israyeli, kuti ndiwakhululukire konse. 7Koma ndidzacitira cifundo
nyumba ya Yuda, ndi kuwapulumutsa mwa Ine Yehova Mulungu
wao, osawapulumutsa ndi uta, kapena lupanga, kapena nkhondo
ndi akavalo, kapena apakavalo. 8Ataleka tsono kuyamwitsa
Wosacitidwa cifundo, anaima, nabala mwana wamwamuna. 9Ndipo
Yehova anati, Umuche dzina lace Si-anthuanga; pakuti inu sindinu
anthu anga, ndipo Ine sindine wanu.

Israyeli acitidwa cifundo

10Angakhale anatero, kuwerenga kwace kwa ana a Israyeli
kudzanga mcenga wa kunyanja, wosayeseka kapena kuwerengeka;
ndipo kudzatero kuti m'mene adawanena, Simuli anthu anga,
adzanena nao, Muli ana a Mulungu wamoyo. 11Ndipo ana a Yuda
ndi ana a Israyeli adzasonkhanidwa pamodzi, nadzadziikira mkuru
mmodzi, nadzakwera kucoka m'dziko; pakuti tsiku la Yezreeli ndi
lalikuru.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Hoseya 2

1Nenani kwa abale anu, Anthu anga, ndi kwa alongo anu,
Wocitidwa-cifundo. 2Mutsutsane naye mai wanu, mutsutsane naye;
pakuti sali mkazi wanga, ndi Ine sindiri mwamuna wace; ndipo
acotse zadama zace pankhope pace, ndi zigololo zace pakati pa
maere ace; 3ndingambvule wamarisece, ndi kumuika ngati tsiku lija
anabadwalo, ndi kumsanduliza ngati cipululu, ndi kumuika ngati
dziko louma, ndi kumupha nalo ludzu; 4ndipo ana ace
sindidzawacitira cifundo; pakuti iwo ndiwo ana acigololo. 5Pakuti
mai wao anacita cigololo; iye amene anali ndi pakati pa iwo anacita
camanyazi; pakuti anati, Ndidzatsata ondikondawo, akundipatsa ine
cakudya canga, ndi madzi anga, ubweya wanga, ndi thonje langa,
mafuta anga, ndi cakumwa canga. 6Cifukwa cace taonani,
ndidzacinga njira yako ndi minga, ndipo ndidzammangira mpanda,
kuti asapeze mabande ace. 7Ndipo adzatsata omkonda koma
osawakumika, adzawafunafuna koma osawapeza; pamenepo adzati,
Ndidzamuka ndi kubwererana ndi mwamuna wanga woyamba,
popeza pamenepo panandikomera koposa tsopano. 8Pakuti
sanadziwa kuti ndine ndinampatsa tirigu, ndi vinyo, ndi mafuta, ndi
kumcurukitsira siliva ndi golidi, zimene anapanga nazo
Baala. 9Cifukwa cace ndidzabwera ndi kucotsa tirigu wanga
m'nyengo yace, ndi vinyo wanga m'nthawi yace yoikika, ndi
kukwatula ubweya wanga ndi thonje langi, zimene zikadapfunda
umarisece wace. 10Ndipo tsopano ndidzaonetsa manyazi ace
pamaso pa omkonda, popandanso wakumlanditsa m'dzanja
langa. 11Ndidzaleketsanso kusekerera kwace konse, madyerero ace,
pokhala mwezi pace, ndi masabata ace, ndi masonkhano ace onse
oikika. 12Ndipo ndidzapasula mipesa yace ndi mikuyu yace, imene
adanena, Iyi ndi mphotho yanga anandipatsa ondikondawo; ndipo
ndidzaisandutsa thengo, ndi nyama zakuthengo zidzaidya. 13Ndipo
ndidzamlanga cifukwa ca masiku a Abaala amene anawafukizira,
nabvala mphete za m'mphuno, ndi zokometsera zace, natsata
omkonda, nandiiwala Ine, ati Yehova. 14Cifukwa cace taonani,
ndidzamkopa ndi kumka naye kucipululu, ndi kulankhula naye
momkonda mtima. 15Ndipo ndidzampatsa minda yace yamphesa
kuyambira pomwepo, ndi cigwa ca Akori cikhale khomo la
ciyembekezo; ndipo adzabvomereza pomwepo monga masiku a
ubwana wace, ndi monga tsiku lokwera iye kuturuka m'dziko la
Aigupto. 16Ndipo kudzakhala tsiku lomwelo, ati Yehova, udzandicha
Mwamuna wanga, osandichanso Baala wanga. 17Pakuti ndidzacotsa
maina a Abaala m'kamwa mwace; ndipo silidzakumbukikanso dzina
lao. 18Ndipo tsiku lomwelo ndidzawacitira pangano ndi nyama za
kuthengo, ndi mbalame za mlengalenga, ndi zokwawa pansi; ndipo
ndidzatyola uta, ndi lupanga, ndi nkhondo, zicoke m'dziko, ndi

kuwagonetsa pansi mosatekeseka. 19Ndipo ndidzakutomera ukhale
wanga kosatha, inde ndidzakutomera ukhale wanga m'cilungamo,
ndi m'ciweruzo, ndi m'ukoma mtima, ndi
m'cifundo. 20Ndidzakutomeranso ukhale wanga mokhulupirika,
ndipo udzadziwa Yehova. 21Ndipo kudzacitika tsiku lomwelo,
ndidzabvomereza, ati Yehova, ndidzabvomereza thambo, ndi ilo
lidzabvomereza dziko lapansi; 22ndi dziko lapansi lidzabvomereza
tirigu, ndi vinyo, ndi mafuta; ndi izi zidzabvomereza
Yezreeli. 23Ndipo ndidzadzibzalira iye m'nthaka, ndipo ndidzacitira
cifundo Wosacitidwa-cifundo; ndipo ndidzati kwa Si-anthu-anga,
Muli anthu anga; ndipo iwo adzati, Ndinu Mulungu wathu.
©The Bible Society of Malawi, 1992

Akwatiranso mkazi woipa, kufaniziranso zocita ana a Israyeli

1Ndipo Yehova anati kwa ine, Mukanso, konda mkazi wokondedwa
ndi bwenzi lace, koma wakucita cigololo monga Yehova akonda ana
a Israyeli, angakhale atembenukira ku milungu yina, nakonda
ncinci za mphesa zouma. 2M'mwemo ndinadzigulira iye ndi
ndalama khumi ndi zisanu zasiliva, ndi homeri ndi nusu wa
barele; 3ndipo ndinati kwa iye, Uzikhala ndi ine masiku ambiri,
usacita cigololo, usakhala mkazi wa mwamuna ali yense;
momwemo inenso nawe. 4Pakuti ana Israyeli adzakhala masiku
ambiri a opanda mfumu, ndi opanda kalonga, ndi opanda nsembe,
ndi opanda coimiritsa, ndi opanda efodi kapena aterafi; 5atatero
ana a Israyeli adzabwera, nadzafuna Yehova Mulungu wao, ndi
Davide mfumu yao, nadzafika ndi mantha kwa Yehova, ndi ku
ukoma wace masiku otsiriza.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Mlandu pakati pa Mulungu ndi Israyeli

1Imvani mau a Yehova, inu ana a Israyeli; pakuti Yehova ali ndi
mlandu ndi okhala m'dziko, popeza palibe coonadi, kapena
cifundo, kapena kudziwa Mulungu m'dziko. 2Koma kulumbira, ndi
kunama, ndi kupha, ndi kuba, ndi kucita cigololo; aboola, ndi
mwazi ukhudzana nao mwazi. 3Cifukwa cace dziko lidzacita cisoni,
ndi ali yense wokhalamo adzalefuka, pamodzi ndi nyama za
kuthengo, ndi mbalame za m'mlengalenga; ndi nsomba za
m'nyanja zomwe zidzacotsedwa. 4Koma munthu asatsutsane ndi
mnzace, kapena kudzudzula mnzace; popeza anthu ako ndiwo
akunga otsutsana ndi wansembe. 5Ndipo udzakhumudwa usana,
ndi mneneri yemwe adzakhumudwa pamodzi ndi iwe usiku; ndipo
ndidzaononga mai wako. 6Anthu anga aonongeka cifukwa ca
kusadziwa; popeza unakana kudziwa, Inenso ndikukaniza, kuti
usakhale wansembe wanga; popeza waiwala cilamulo ca Mulungu
wako, Inenso ndidzaiwala ana ako. 7Monga anacuruka, momwemo
anandicimwira; ndidzasanduliza ulemerero wao ukhale
manyazi. 8Adyerera cimo la anthu anga, nakhumbira cosalungama
cao, yense ndi mtima wace. 9Ndipo kudzakhala monga anthu,
momwemo wansembe; ndipo ndidzawalanga cifukwa canjira zao,
ndi kuwabwezera macitidwe ao. 10Ndipo adzadya, koma osakhuta;
adzacita cigololo, koma osacuruka; pakuti waleka kusamalira
Yehova. 11Cigololo, ndi vinyo, ndi vinyo watsopano, zicotsa
mtima, 12Anthu anga afunsira ku mtengo wao, ndi ndodo yao
iwafotokozera; pakuti mzimu wacigololo wawalakwitsa, ndipo acita
cigololo kucokera Mulungu wao. 13Pamwamba pa mapiri aphera
nsembe, nafukiza pazitunda, patsinde pa thundu, ndi miniali, ndi
mkundi; popeza mthunzi wace ndi wabwino, cifukwa cace ana anu
akazi acita citole, ndi apongozi anu acita cigololo. 14Sindidzalanga
ana anu akazi pocita citole iwo, kapena apongozi anu pocita
cigololo iwo; pakuti iwo okha apambukira padera ndi akazi acitole,
naphera nsembe pamodzi ndi akazi operekedwa kucitole; ndi
anthu osazindikirawo adzagwetsedwa camutu. 15Cinkana iwe,
Israyeli, ucita citole, koma asaparamule Yuda; ndipo musafika inu
ku Giligala, kapena kukwera ku Betaveni, kapena kulumbira, Pali
Yehova. 16Pakuti Israyeli wacita kuuma khosi ngati ng'ombe yaikazi
yaing'ono youma khosi; tsopano Yehova adzawadyetsa ngati
mwana wa nkhosa ku thengo lalikuru. 17Efraimu waphatikana ndi
mafano, mlekeni. 18Cakumwa cao casasa, acita citole kosalekeza;
akuru ao akonda manyazi kwambiri. 19Mphepo yamkulunga
m'mapiko ace, ndipo adzacita manyazi cifukwa ca nsembe zao.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Kulowerera kwa Israyeli

1Imvani ici, ansembe inu; mverani, inu nyumba ya Israyeli; cherani
khutu, inu nyumba ya mfumu; pakuti ciweruzoci cinena inu; pakuti
munakhala msampha ku Mizipa, ndi ukonde woyalidwa pa
Tabora. 2Ndipo opandukawo analowadi m'zobvunda; koma Ine
ndine wakuwadzudzula onsewo. 3Ndimdziwa Efraimu, ndi Israyeli
sandibisikira; pakuti Efraimu iwe, wacita citole tsopano, Israyeli
wadetsedwa. 4Macitidwe ao sawalola kubwerera kwa Mulungu
wao; pakuti mzimu wacitole uli m'kati mwao, ndipo sadziwa
Yehova. 5Ndipo kudzikuza kwa Israyeli kudzamcitira umboni
pamaso pace; cifukwa cace Israyeli ndi Efraimu adzakhumudwa
m'mphulupulu mwao; Yudanso adzakhumudwa pamodzi
nao. 6Adzamuka ndi zoweta zao zazing'ono ndi zazikuru
kufunafuna Yehova: koma sadzampeza; Iye wadzibweza
kuwacokera. 7Anacita mosakhulupirika pa Yehova, pakuti anabala
ana acilendo; mwezi wokhala udzawatha tsopano, pamodzi ndi
maiko ao.
8Ombani mphalasa m'Gibeya, ndi lipenga m'Rama; pfuulani ku
Betaveni; pambuyo pako, Benjamini. 9Efraimu adzasanduka bwinja
tsiku lakudzudzula; mwa mapfuko a Israyeli ndadziwitsa
codzacitikadi. 10Akalonga a Yuda akunga anthu osuntha malire;
ndidzawatsanulira mkwiyo wanga ngati madzi. 11Efraimu azunzika,
apsinjika pa mlanduwo; pakuti anafuna mwini wace kutsata
lamulolo. 12Ndipo ndikhala kwa Efraimu ngati njenjete, ndi kwa
nyumba ya Yuda ngati cibvundi. 13Pamene Efraimu anaona
nthenda yace, ndi Yuda bala lace, Efraimu anamuka kwa Asuri,
natumiza kwa mfumu Yarebu; koma iye sakhoza kukuciritsani,
kapena kupoletsa bala lanu. 14Pakuti ndidzakhala kwa Efraimu
ngati mkango, ndi kwa nyumba ya Yuda ngati msona wa mkango;
ndidzamwetula Ine ndi kucoka; ndidzanyamula, ndipo palibe
wakulanditsa. 15Ndidzamuka ndi kubwerera kumka kumalo
kwanga, mpaka adzabvomereza kuparamula kwao, nafunafuna
nkhope yanga; m'msauko mwao adzandifunafuna mwacangu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Israyeli abwerera kunka kwa Yehova

1Tiyeni, tibwerere kunka kwa Yehova; pakuti wang'amba,
nadzatipoletsera; wakantha, nadzatimanga. 2Atapita masiku awiri
adzatitsitsimutsa, tsiku lacitatu adzatiutsa; ndipo tidzakhala ndi
moyo pamaso pace. 3Tidziwe tsono, tilondole kudziwa Yehova;
kuturuka kwace kwakonzekeratu ngati matanda kuca; ndipo
adzatidzera ngati mvula, ngati mvula ya masika yakuthirira dziko.

Efraimu ndi Yuda adrudzulidwa

4Efraimu iwe, ndidzakucitira ciani? Yuda iwe, ndikucitire ciani?
pakuti kukoma mtima kwako kukunga mtambo wam'mawa ndi
ngati mame akuphawa mamawa. 5Cifukwa cace ndawalikha mwa
aneneri; ndawapha ndi mau a pakamwa panga; ndi maweruzo
anga aturuka ngati kuunika. 6Pakuti ndikondwera naco cifundo, si
nsembe ai; ndi kumdziwa Mulungu koposa nsembe
zopsereza. 7Koma iwo analakwira cipangano ngati Adamu, m'mene
anandicitira monyenga. 8Gileadi ndiwo mudzi wa ocita zoipa, wa
mapazi a mwazi. 9Ndipo monga magulu a mbala alalira munthu,
momwemo msonkhano wa ansembe amapha pa njira ya ku
Sekemu; indedi acita coipitsitsa. 10M'nyumba ya Israyeli ndinaona
cinthu coopsetsa; pamenepo pali citole ca Efraimu; Israyeli
wadetsedwa. 11Akuikidwiratunso nyengo yakukolola, Yuda iwe,
pamene ndikabwezanso undende wa anthu anga.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Kucimwa ndi kupandukira kwa Israyeli

1M'mene ndiciritsa Israyeli, mphulupulu ya Efraimu ibvumbuluka,
ndi zoipa za Samariya; pakuti acita bodza, ndipo mkhungu alowa
m'nyumba, ndi gulu la mbala manca kubwalo. 2Ndipo sanena
m'mtima mwao kuti Ine ndikumbukila zoipa zao zonse; tsopano
macitidwe ao awazinga; ali pamaso panga, 3Akondweretsa mfumu
ndi zoipa zao, ndi akalonga ndi mabodza ao. 4Acigololo onsewo;
akunga ng'anjo anaitenthetsa wooca mkate; aleka kusonkha moto,
poyambira kukanda mtanda kufikira watupa mtandawo. 5Tsiku la
mfumu yathu akalonga adzidwalitsa ndi kutentha kwa vinyo; iye
anatambasula dzanja lace pamodzi ndi oseka. 6Pakuti asendera
nao mtima wao wakunga ng'anjo ya mkate, pokhala alikulalira;
wooca mkate wao agona usiku wonse, m'mawa iyaka ngati moto
wa malawi. 7Onsewo atentha ngati ng'anjo, natha oweruza ao,
agwa mafumu ao onse; palibe mmodzi mwa iwo wakuitana
Ine. 8Efraimu asokonezana nayo mitundu ya anthu; Efraimu ndiye
kamtanda ka mkate kosatembenuzidwa. 9Alendo anatha mphamvu
yace osacidziwaiye; imvi zomwe zampakiza osacidziwa
iye, 10Ndipo kudzikuza kwa Israyeli kumcitira umboni pamaso
pace; koma sanabwerera kumka kwa Yehova Mulungu wao, kapena
kumfunafuna mwa ici conse. 11Ndipo Efraimu ali ngati nkhunda
yopusa yopanda nzeru; aitanira kwa Aigupto, amuka kwa
Asuri. 12Pamene amuka ndidzawayalira ukonde wanga,
ndidzawagwetsa ngati mbalame za m'mlengalenga,
ndidzawalanga monga udamva msonkhano wao. 13Tsoka kwa
iwowa! pakuti anandizembera; cionongeko kwa iwowa! pakuti
anandilakwira; ndikadawalanditsa Ine, koma anandinenera
zabodza. 14Ndipo sanapfuulira kwa Ine ndi mtima wao, koma alira
pakama pao, asonkhanira tirigu ndi vinyo, apikisana ndi
Ine. 15Cinkana ndawalangiza ndi kulimbitsa manja ao,
andilingiririra coipa, 16Abwerera, koma si kwa Wam'mwambayo;
akunga uta wosakhulupirika; akalonga ao adzagwa ndi lupanga
mwa cipongwe ca lilime lao; ici ndico adzawasekera m'dziko la
Aigupto.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Kupembedza mafano ndi kusamvera kwa Israyeli

1Lipenga kukamwa kwako, Akudza ngati ciombankhanga, kulim
bana ndi nyumba ya Yehova; cifukwa analakwira cipangano canga,
napikisana naco cilamulo canga. 2Adzapfuulira kwa Ine, Mulungu
wanga, ife Aisrayeli tikudziwani. 3Israyeli wacitaya cokoma, mdani
adzamlondola. 4Analonga mafumu, koma sikunacokera kwa Ine;
anaika akalonga, koma sindinadziwa; anadzipangira mafano a
siliva wao ndi golidi wao, kuti akalikhidwe. 5Mwana wa ng'ombe
wako wakutaya, Samariya iwe; mkwiyo wanga wayakira iwo;
adzalephera kuyera mtima mpaka liti? 6Pakuti ici comwe cafumira
kwa Israyeli; mmisiri wampanga, koma sali Mulungu; inde mwana
wa ng'ombe wa Samariya adzaphwanyika-phwanyika. 7Pakuti
abzala mphepo, nadzakolola kabvumvulu; alibe tirigu wosasenga;
ngala siidzaturutsa ufa; cinkana iuturutsa, alendo
adzaumeza. 8Israyeli wamezedwa; tsopano ali mwa amitundu ngati
cotengera coti munthu sakondwera naco. 9Pakuti anakwera kumka
ku Asuri, ngati mbidzi ya pa yokha mwini wace; Efraimu
walembera omkonda ngati anchito. 10Inde angakhale alembera
mwa amitundu ndidzawasonkhanitsa tsopano; ndipo ayamba
kucepa cifukwa ca katundu wa mfumu ya akalonga. 11Popeza
Efraimu anacurukitsa maguwa a nsembe akucimwako, maguwa a
nsembe omwewo anamcimwitsa. 12Ndinamlembera zinthu
zambirimbirizo za cilamulo canga, koma zinayesedwa ngati cinthu
cacilendo. 13Kunena za nsembe za zopereka zanga, aphera
nsembe yanyama, naidya; koma Yehova sazilandira; tsopano
adzakumbukila mphulupulu yao, nadzalanga zocimwa zao;
adzabwerera kumka ku Aigupto. 14Pakuti Israyeli waiwala Mlengi
wace, namanga akacisit ndipo Yuda wacurukitsa midzi yamalinga;
koma ndidzatumizira midzi yace moto, nudzatha nyumba zace
zazikuru.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Cimo la Israyeli ndi zotsatira zace

1Usakondwera, Israyeli, ndi kusekerera, ngati mitundu ya anthu;
pakuti wacita cigololo kuleka Mulungu wako, wakonda mphotho ya
cigololo pa dwale la tirigu liri lonse. 2Dwale ndi coponderamo
mphesa sizidzawadyetsa, vinyo watsopano
adzamsowa. 3Sadzakhala m'dziko la Yehova; koma Efraimu adza
bwerera kumka ku Aigupto; ndipo adzadya cakudya codetsa
m'Asuri. 4Sadzatsanulira Yehova nsembe zavinyo; sizidzamkomera
Iye nsembe zao; zidzakhala kwa iwo ngati mkate wa acisoni; onse
akudyako adzadetsedwa; pakuti mkate wao udzakhala wa njala
yao, uwu sudzalowa m'nyumbaya Yehova. 5Mudzacitanji tsiku la
masonkhano oikika, ndi tsiku la madyerero a Yehova? 6Pakuti
taonani, anacokera cionongeko, koma Aigupto adzawasonkhanitsa,
Mofi adzawaika m'manda; khwisa adzalanda zofunika zao zasiliva;
minga idzakhala m'mahema mwao. 7Masiku a kulanga afika,
masiku a kubwezera afika; Israyeli adzadziwa; mneneri ali wopusa,
munthu wamzimu ali wamisala, cifukwa ca kucuruka mphulupulu
yako, ndi popeza udani ndi waukuru. 8Efraimu ndiye wozonda kwa
Mulungu wanga; kunena za mneneri, msampha wa msodzi uli
m'njira zace zonse, ndi udani m'nyumba ya Mulungu
wace. 9Anadzibvunditsa kwambiri, monga masiku a Gibeya;
adzakumbukila mphulupulu yao, adzalanga zocimwa
zao. 10Ndinapeza Israyeli ngati mphesa m'cipululu, ndinaona
makolo anu ngati cipatso coyamba ca mkuyu nyengo yace
yoyamba; koma anadza kwa Baala Peori, nadzipatulira
conyansaco, nasandulika onyansa, conga cija
anacikonda. 11Kunena za Efraimu, ulemerero wao udzauluka ndi
kucoka ngati mbalame; sipadzakhala kubala, ndi kukhala ndi
pakati, ndi kuima. 12Angakhale alera ana ao, koma
ndidzawasowetsa, wosatsala munthu; ndithunso tsoka iwowa,
pamene ndiwacokera. 13Efraimu, monga ndaona, akunga Turo,
wookedwa pokoma; koma Efraimu adzaturutsira ana ace
wakuwaphera. 14Apatseni, Yehova; mudzapatsa ciani? muwapatse
mimba yotayataya, ndi mawere ouma. 15Coipa cao conse ciri
m'Giligala; pakutipamenepo ndinawada, cifukwa ca kuipa kwa
macitidwe ao ndidzawainga kuwacotsa m'nyumba mwanga;
sindidzawakondanso; akalonga ao onse ndiwo opanduka. 16Efraimu
wakanthidwa, muzu wao wauma, iwo sadzabala zipatso; inde
ngakhale abala, koma ndidzapha zipatso zofunika za mimba
yao. 17Mulungu wanga adzawataya, pakuti sanammvera Iye; ndipo
adzakhala othawathawa mwa amitundu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Hoseya 10

1Israyeli ndi mpesa wotambalala, wodzibalira wokha zipatso; monga umo
zinacurukira zipatso zace, momwemo anacurukitsa maguwa a nsembe ace;
monga mwa kukoma kwace kwa dziko lace anapanga zoimiritsa
zokoma. 2Mtima wao wagawikana, tsopano adzapezeka oparamula, adzapasula
maguwa ao a nsembe, nadzaononga zoimiritsa zao. 3Pakuti tsopano adzati,
Tiribe mfumu, popeza sitiopa Yehova; ndi mfumu idzaticitira ciani? 4Anena mau
akulumbira monama, pakucita mapangano momwemo; ciweruzo ciphuka ngati
zitsamba zowawa m'micera ya munda. 5Okhala m'Samariya adzaopera cifanizo
ca ana a ng'ombe a ku Betaveni; pakuti anthu ace adzamva naco cisoni, ndi
ansembe ace amene anakondwera naco, cifukwa ca ulemerero wace, popeza
unacicokera. 6Adzacitengeranso ku Asuri cikhale mphatso ya kwa mfumu
Yarebu; Efraimu adzatenga manyazi, ndi Israyeli adzacita manyazi ndi uphungu
wace. 7Ndipo Samariya, mfumu yace yamwelera ngati thobvu pamadzi. 8Ndipo
misanje ya Aveni, ndiyo cimo la Israyeli, idzaonongeka; minga ndi mitungwi
idzamera pa maguwa ao a nsembe; ndipo adzati kwa mapiri, Tiphimbeni; ndi
kwa zitunda, Tigwereni. 9Israyeli, wacimwa kuyambira masiku a Gibeya;
pomwepo anaimabe; nkhondo ya pa ana a cosalungama siinawapeza ku
Gibeya. 10Pamene ndifuna ndidzawalanga, ndi mitundu ya anthu
idzawasonkhanira pomangidwa iwo pa zolakwa zao ziwiri. 11Ndipo Efraimu
ndiye ng'ombe yaikazi yaing'ono, yozereweredwa, yokonda kupuntha tirigu;
koma ndapita pa khosi lace lokoma; ndidzamsenzetsa Efraimu goli; Yuda
adzalima, Yakobo adzaphwanya cibuluma cace. 12Mudzibzalire m'cilungamo
mukolole monga mwa cifundo; limani masala anu, pakuti yafika nthawi ya
kufuna Yehova, mpaka afika Iye, nabvumbitsira inu cilungamo. 13Mwalima
coipa, mwakolola cosalungama, mwadya zipatso za mabodza; pakati watama
njira yako ndi kucuruka kwa anthu ako amphamvu. 14Momwemo phokoso
lidzaukira anthu ako, ndi malinga ako onse adzapasuka, monga Salimani
anapasula Betaribeli; tsiku la nkhondo amai anaphwanyika pamodzi ndi ana
ace. 15Momwemo adzakucitirani Betele, cifukwa ca coipa canu cacikuru;
mbanda kuca mfumu ya Israyeli idzalikhika konse.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Kusayamika kwa Israyeli; macenjezo ndi malonjezo

1Pamene Israyeli anali mwana, ndinamkonda, ndinaitana mwana
wanga ali m'Aigupto. 2Monga anawaitana, momwemo
anawacokera; anaphera nsembe Abaala, nafukizira mafano
osema. 3Koma Ine ndinaphunzitsa Efraimu kuyenda,
ndinawafungata m'manja mwanga; koma sanadziwa kuti
ndinawaciritsa. 4Ndinawakoka ndi zingwe za munthu, ndi
zomangira za cikondi; ndinakhala nao ngati iwo akukweza goli
pampuno pao, ndipo ndinawaikira cakudya. 5Iye sadzabwerera
kumka ku dziko la Aigupto, koma Asuri adzakhala mfumu yace,
popeza anakana kubwera. 6Ndi lupanga lidzagwera midzi yace,
lidzatha mipiringidzo yace, ndi kuononga cifukwa ca uphungu
wao. 7Ndipo anthu anga alimbika kubwerera m'mbuyo kundileka
Ine; cinkana akawaitana atsate Iye ali m'mwamba, sadzakweza ndi
mmodzi yense. 8Ndidzakusiya bwanji, Efraimu? ndidzakupereka
bwanji, Israyeli? ndidzakuyesa bwanji ngati Adima? ndidzakuika
bwanji ngati Zeboimu? mtima wanga watembenuka m'kati
mwanga, zacifundo zanga zilira zonse pamodzi. 9Sindidzacita
mkwiyo wanga waukali, sindidzabwerera kuononga Efraimu; pakuti
Ine ndine Mulungu, si munthu ai; Woyera wa pakati pako; ndipo
sindidzalowa m'mudzi. 10Adzatsata Yehova, Iye adzabangula ngati
mkango; pamene abangula, ana adzafika ndi kunjenjemera
kucokera kumadzulo. 11Adzafika ndi kunjenjemera ngati mbalame
ya ku Aigupto, ndi ngati nkhunda m'dziko la Asuri; ndipo
ndidzawakhalitsa m'nyumba zao, ati Yehova.
12Efraimu andizinga ndi bodza, ndi nyumba ya Israyeli ndi
cinyengo, ndi Yuda apikisana ndi Mulungu, ndiye Woyera
wokhulupirika.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Mlandu wa Yehova pa Israyeli ndi Yuda

1Efraimu akudya mphepo, natsata mphepo ya kum'mawa; tsiku
lonse acurukitsa mabodza ndi cipasuko, ndipo acita pangano ndi
Asuri, natenga mafuta kumka nao ku Aigupto, 2Ndipo Yehova ali
ndi mlandu ndi Yuda, nadzalanga Yakobo monga mwa njira zace,
adzambwezera monga mwa macitidwe ace. 3M'mimba anagwira ku
citende ca mkuru wace, ndipo atakula mphamvu analimbana ndi
Mulungu; 4inde, analimbana ndi wamthenga nampambana;
analira, nampembedza Iye; anampeza Iye ku Beteli, ndi kumeneko
Iye analankhula ndi ife; 5ndiye Yehova Mulungu wa makamu,
cikumbukilo cace ndi Yehova. 6M'mwemo utembenukire kwa
Mulungu wako, sunga cifundo ndi ciweruzo, nuyembekezere
Mulungu wako kosalekeza. 7Ndiye Mkanani, m'dzanja lace muli
miyeso yonyenga, akonda kusautsa. 8Ndipo Efraimu anati, Zedi
ndasanduka wolemera, ndadzionera cuma m'nchito zonse
ndinazigwira; sadzapeza mwa ine mphulupulu yokhala
cimo. 9Koma Ine ndine Yehova Mulungu wako cicokere dziko la
Aigupto, ndidzakukhalitsanso m'mahema, monga masiku a
masonkhano oikika. 10Ndalankhulanso ndi aneneri, ndipo Ine
ndacurukitsa masomphenya; ndi pa dzanja la aneneri ndinanena
ndi mafanizo. 11Kodi Gileadi ndiye wopanda pace? akhala acabe
konse; m'Giligala aphera nsembe yang'ombe; inde maguwa ao a
nsembe akunga miulu yamiyala m'micera ya munda. 12Ndipo
Yakobo anathawira ku thengo la Aramu, ndi Israyeli anagwira
nchito cifukwa ca mkazi, ndi cifukwa ca mkazi anaweta
nkhosa. 13Ndipo mwa mneneri Yehova anakweretsa Israyeli
kucokera m'Aigupto, ndi mwa mneneri anasungika. 14Efraimu
wautsa mkwiyo wowawa, m'mwemo Iye adzamsiyira mwazi wace,
ndi Ambuye wace adzambwezera comtonza cace.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Cimo la Israyeli ndi kulangidwa kwace

1Pamene Bfraimu analankhula panali kunjenjemera; anadzikweza
m'Israyeli; koma pamene anaparamula mwa Baala, anafa. 2Ndipo
tsopano aonjeza kucimwa, nadzipangira mafano oyenga a siliva
wao, mafano monga mwa nzeru zao, onsewo nchito ya amisiri;
anena za iwo, Anthu ophera nsembe apsompsone ana a
ng'ombe. 3Cifukwa cace adzakhala ngati mtambo wa m'mawa, ndi
ngati mame asansuka mamawa, ngati mungu umene mphepo
iuuluza kudwale, ndi ngati utsi woturuka kukafwambira. 4Koma Ine
ndine Yehova Mulungu wako cicokere m'dziko la Aigupto, ndipo
suyenera kudziwa mulungu wina koma Ine; ndi popanda Ine palibe
mpulumutsi. 5Ndinakudziwa m'cipululu, m'dziko lotentha
kwambiri. 6Monga mwa podyetsa pao, momwemo anakhuta;
anakhuta, ndi mtima wao unakwezeka; cifukwa cace anandiiwala
Ine. 7Cifukwa cace ndikhala nao ngati mkango; ngati nyalugwe
ndidzalalira kunjira. 8Ndidzakomana nao ngati cimbalangondo
cocilanda ana ace, ndi kung'amba cokuta mtima wao; ndi
pomwepo ndidzawalusira ngati mkango; cirombo
cidzawamwetula. 9Israyeli, cikuononga ndi ici, cakuti utsutsana ndi
Ine, cithandizo cako. 10Iri kuti mfumu yako tsopano, kuti
ikupulumutse m'midzi yako yonse? ndi oweruza ako amene
unanena za iwo, Ndipatseni mfumu ndi akalonga? 11Ndinakupatsa
mfumu mu mkwiyo wanga; ndinamcotsanso m'ukali
wanga. 12Mphulupulu ya Efraimu yamangika, cimo lace
lisungika. 13Zowawa zonga za mkazi wobala zidzamgwera, ndiye
mwana wopanda nzeru; pakuti pali nyengo yakuti asacedwe
mobalira ana. 14Ndidzawaombola ku, mphamvu ya kumanda,
ndidzawaombola kuimfa; imfa, miliri yako iri kuti? manda,
cionongeko cako ciri kuti? Kulekerera kudzabisika pamaso
panga. 15Cinkana abala mwa abale ace, mphepo ya kum'mawa
idzafika, mphepo ya Yehova yokwera kucokera kucipululu; ndi
gwero lace lidzaphwa, ndi kasupe wace adzauma, adzafunkha
cuma ca akatundu onse ofunika. 16Samariya adzasanduka
wabwinja, pakuti anapandukana ndi Mulungu wace; iwo adzagwa
ndi lupanga, ana ao amakanda adzaphwanyika, ndi akazi ao okhala
ndi pakati adzatumbulidwa.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Mulungu adandaulira Israyeli alape, nalonjeza kuwakhululukira

1Israyeli, bwerera kumka kwa Yehova Mulungu wako; pakuti wagwa
mwa mphulupulu yako. 2Mukani nao mau, nimubwerere kwa
Yehova; nenani kwa Iye, Cotsani mphulupulu zonse, nimulandire
cokoma; ndipo tidzapereka mau milomo yathu ngati:
ng'ombe. 3Asuri sadzatipulumutsa; sitidzayenda pa akavalo, ndipo
sitil dzanenanso kwa nchito ya manja athu, Inu ndinu milungu
yathu; pakuti mwa Inu ana amasiye apeza cifundo. 4Ndidzaciritsa
kubwerera kwao, ndidzawakonda mwaufulu; pakuti mkwiyo wanga
wamcokera. 5Ndidzakhala kwa Israyeli ngati mame; adzacita
maluwa ngati kakombo, ndi kutambalalitsa mizu yace ngati
Lebano. 6Nthambi zace zidzatambalala, ndi kukoma kwace
kudzanga kwa mtengo waazitona, ndi pfungo lace ngati
Lebano. 7Iwo okhala pansi pa mthunzi wace adzabwera,
nadzatsitsimuka ngati tirigu, nadzaphuka ngati mpesa,
cikumbukilo cace cidzanga vinyo wa Lebano. 8Efraimu adzati, Ndiri
ndi cianinso ndi mafano? Ndayankha, ndidzampenyerera; ndiri
ngati mtengo wamlombwa wabiriwiri; zipatso zako zipezeka
zocokera kwa Ine. 9Wanzeru ndani, kuti azindikire izi? waluntha,
kuti adziwe izi? pakuti njira za Yehova ziri zoongoka; ndipo
olungama adzayendamo, koma olakwa adzagwamo.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Joel

Yoweli 1

Tsoka locokera ku dzombe ndi cirala

1MAU a Yehova a kwa Yoeli mwana wa Petueli.
2Imvani ici, akulu akulu inu, nimuchere khutu, inu nonse okhala
m'dziko. Cacitika ici masiku anu kodi, kapena masiku a makolo
anu? 3Mufotokozere ana anu ici, ndi ana anu afotokozere ana ao,
ndi ana ao afotokozere mbadwo wina. 4Cosiya cimbalanga,
dzombe lidacidya; ndi cosiya dzombe, cirimamine adacidya; ndi
cosiya cirimamine, anoni adacidya. 5Galamukani, oledzera inu,
nimulire; bumani, nonse akumwa vinyo, cifukwa ca vinyo
watsopano; pakuti waletsedwa pakamwa panu. 6Pakuti mtundu
wadza, wakwerera dziko langa, wamphamvu wosawerengeka,
mano ace akunga mano a mkango, nukhala nao mano acibwano a
mkango waukuru. 7Unaonongadi mpesa wanga, nunyenya mkuyu
wanga, nuukungudza konse, nuutaya; nthambi zace zasanduka
zotumbuluka. 8Lirani ngati namwali wodzimangira m'cuuno
ciguduli, cifukwa ca mwamuna wa unamwali wace. 9Nsembe yaufa
ndi nsembe yothira zalekeka ku nyumba ya Yehova; ansembe,
atumiki a Yehova, acita maliro. 10M'munda mwaonongeka, nthaka
ilira; pakuti tirigu waonongeka, vinyo watsopano wamwelera,
mafuta akudza pang'onong'ono. 11Gomani, akulima m'minda inu;
lirani, akulima mpesa; cifukwa ca tirigu ndi barele; pakuti dzinthu
za m'minda zatayika. 12Mpesa wauma, mkuyu wafota, mtengo wa
mkangaza ndi kanjedza ndi muula, inde mitengo yonse ya
kuthengo yafota; pakuti cimwemwe cathera ana a
anthu. 13Mudzimangire ciguduli m'cuuno mwanu, nimulire
ansembe inu; bwnani, otumikira ku guwa la nsembe inu; lowani,
gonani usiku wonse m'ciguduli, inu otumikira Mulungu wanga;
pakuti nsembe yaufa ndi nsembe yothira zaletsedwera nyumba ya
Mulungu wanu. 14Patulani tsiku losala, lalikirani masonkhano
oletsa, sonkhanitsani akulu akulu, ndi onse okhala m'dziko, ku
nyumba ya Yehova Mulungu wanu; nimupfuulire kwa
Yehova. 15Kalanga ine, tsikuli! pakuti layandikira tsiku la Yehova,
lidzafika ngati cionongeko cocokera kwa
Wamphamvuyonse. 16Cakudya sicicotsedwa kodi pamaso pathu?
cimwemwe ndi cikondwerero pa nyumba ya Mulungu
wathu? 17Mbeu zaola pansi pa zibuluma zao; zosungiramo
zaonongeka, nkhokwe zapasuka; pakuti tirigu wakwinyata. 18Ha!
nyama ziusa moyo, magulu a ng'ombe azimidwa; pakuti zisowa
podyera; magulu a nkhosa omwe atha. 19Ndipfuulira kwa Inu
Yehova, pakuti moto wapsereza mabusa a m'cipululu, ndi malawi a
moto anatentha mitengo yonse ya kuthengo, 20inde nyama za

kuthengo zilira kwa Inu; pakuti mitsinje yamadzi yaphwa, ndi moto wapsereza mabusa a m'cipululu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Cilango coopsa ca Mulungu

1Muombe lipenga m'Ziyoni, nimupfuulitse m'phiri langa lopatulika;
onse okhala m'dziko anjenjemere; pakuti tsiku la Yehova lirinkudza,
pakuti liyandikira; 2tsiku la mdima, la mdima wandiweyani, tsiku la
mitambo, mitambo yocindikira, ngati m'mbandakuca moyalika
pamapiri; mtundu waukuru ndi wamphamvu, panalibe wotere ndi
kale lonse, sipadzakhalanso wotere utapita uwu, kufikira zaka za
mibadwo yambiri. 3Moto unyambita pamaso pao, ndi m'mbuyo
mwao litentha lawi la moto; kumaso kwao dziko likunga munda wa
Edeni, koma m'mbuyo mwao likunga cipululu copanda kanthu;
palibenso wakuwapulumuka. 4Maonekedwe ao aoneka ngati
akavalo, nathamanga ngati akavalo a nkhondo. 5Atumphako ngati
mkokomo wa magareta pamwamba pa mapiri, ngati kulilima kwa
malawi a moto akupsereza ziputu, ngati mtundu wamphamvu wa
anthu ondandalikira nkhondo. 6Pamaso pao mitundu ya anthu
ikumva zowawa, nkhope zonse zitumbuluka. 7Athamanga ngati
amphamvu; akwera linga ngati anthu a nkhondo; niliyenda liri
lonse njira yace, osasokonezeka m'mabande ao. 8Sakankhana,
ayenda liri lonse m'mopita mwace; akagwa m'zida, siityoka
nkhondo yao. 9Alumphira mudzi, athamanga palinga, akwerera
nyumba, alowera pamazenera ngati mkhungu. 10Dziko lapansi
linjenjemera pamaso pao, thambo ligwedezeka, dzuwa ndi mwezi
zada, ndi nyenyezi zi'bweza kuwala kwao; 11ndipo Yehova
amveketsa mau ace pamaso pa khamu lace la nkhondo; pakuti a
m'cigono mwace ndi ambirimbiri; pakuti Iye wakucita mau ace
ndiye wamphamvu ndithu; pakuti tsiku la Yehova ndi lalikuru ndi
loopsa ndithu; akhoza kupirira nalo ndani? 12Koma ngakhale
tsopano, ati Yehova, munditembenukire Ine ndi mtima wanu
wonse, ndi kusala, ndi kulira, ndi kucita maliro; 13ndipo ng'ambani
mitima yanu, si zobvala zanu ai; ndi kurembenukira kwa Yehova
Mulungu wanu; pakuti Iye ndiye wacisomo, ndi wodzala cifundo,
wosapsa mtima msanga, ndi wocuruka kukoma mtima, ndi woleka
coipaco. 14Kaya, kapena adzabwerera, nadzalekerera, ndi kusiya
mdalitso pambuyo pace, ndiwo nsembe yaufa ndi nsembe yathira
ya Yehova Mulungu wanu.
15Ombani lipenga m'Ziyoni, patulani tsiku losala, lalikirani
msonkhano woletsa, 16sonkhanitsani anthu, patulani msonkhano,
memezani akulu akulu, sonkhanitsani ana ndi oyamwa mawere;
mkwati aturuke m'cipinda mwace, ndi mkwatibwi m'mogona
mwace. 17Ansembe, atumiki a Yehova, alire pakati pa khonde la
pakhomo ndi guwa la nsembe, nanene, Alekeni anthu anu, Yehova,
musapereka colowa canu acitonze, kuti amitundu awalamulire;
adzaneneranji mwa anthu, Ali kuti Mulunguwao?

Lonjezo lakuti cidzacuruka cakudya

18Pamenepo Yehova anacitira dziko lace nsanje, nacitira anthu ace
cifundo. 19Ndipo Yehova anayankha, nati kwa anthu ace, Taonani,
ndidzakutumizirani tirigu, ndi vinyo, ndi mafuta; ndipo mudzakhuta
ndi izo; ndipo sindidzakuperekaninso mukhale citonzo mwa
amitundu; 20koma ndidzakucotserani kutali nkhondo ya kumpoto,
ndi kulingira ku dziko louma ndi lopasuka, a kumaso kwace ku
nyanja ya kum'mawa, ndi a kumbuyo kwace ku nyanja ya
kumadzulo; ndi kununkha kwace kudzakwera, ndi pfungo lace loipa
lidzakwera; pakuti inacita zazikuru. 21Usaopa, dziko iwe; kondwera,
nusekerere; pakuti Yehova wacita zazikuru. 22Musamaopa, nyama
za kuthengo inu; pakuti m'cipululu muphukanso msipu; pakuti
mitengo ibala zipatso zao; mikuyu ndi mipesa ipatsa mphamvu
zao. 23Mukondwere tsono, inu ana a Ziyoni, nimusekerere
m'Yehova Mulungu wanu; pakuti adzayamba kukupatsani mvula
yamyundo, monga mwa cilungamo cace; nakubvumbitsirani
mvula, mvula yamyundo ndi yamasika mwezi woyamba. 24Ndipo
madwale adzakhala ndi tirigu, ndi vinyo, ndi mafuta; zidzasefuka
m'zosungiramo zao. 25Ndipo ndidzakubwezerani zaka zidazidya
dzombe, ndi cirimamine, ndi anoni, ndi cimbalanga, gulu langa
lalikuru la nkhondo, limene ndinalitumiza pakati pa inu. 26Ndipo
mudzadyaidya ndi kukhuta, nimudzalemekeza dzina la Yehova
Mulungu wanu, amene anacita nanu modabwiza; ndi anthu anga
sadzacita manyazi nthawi zonse. 27Ndipo mudzadziwa kuti Ine ndiri
pakati pa Israyeli, ndi kuti Ine ndine Yehova Mulungu wanu, palibe
wina; ndi anthu anga sadzacita manyazi nthawi zonse.
28Ndipo kudzacitika m'tsogolo mwace, ndidzatsanulira mzimu
wanga pa anthu onse, ndi ana anu amuna ndi akazi adzanenera,
akulu akulu anu adzalota maloto, anyamata anu adzaona
masomphenya; 29ndi pa akapolo ndi adzakazi omwe
ndidzatsanulira mzimu wanga masiku awo. 30Ndipo ndidzaonetsa
zodabwiza kuthambo ndi pa dziko lapansi, mwazi, ndi moto, ndi
utsi tolo. 31Dzuwa lidzasanduka mdima, ndi mwezi udzasanduka
mwazi, lisanadze tsiku la Yehova lalikuru ndi loopsa. 32Ndipo
kudzacitika kuti ali yense adzaitana pa dzina la Yehova
adzapulumutsidwa; pakuti m'phiri la Ziyoni ndi m'Yerusalemu
mudzakhala cipulumutso, monga Yehova anatero, ndi mwa otsala
amene Yehova adzawaitana.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Aneneratu za cilango ca Mulungu pa adani ace; Israyeli adzakonrekanso

1Pakuti taonani, masiku awo, ndi nthawi iyo, pamene ndibwera nao
andende a Yuda ndi a Yerusalemu, 2ndidzasonkhanitsa amitundu
onse, ndi kutsikira nao ku cigwa ca Yosafati; ndipo ndidzaweruzana
nao komweko za anthu anga, ndi colowa canga Israyeli, amene
anawabalalitsa mwa amitundu, nagawa dziko langa, 3Ndipo
anacitira anthu anga maere, napereka mwana wamwamuna
kusinthana ndi mkazi wadama, nagula vinyo ndi mwana wamkazi
kuti amwe. 4Ndiponso ndiri ndi ciani ndi inu, Turo ndi Zidoni, ndi
malire onse a Afilisti? mudzandibwezera cilango kodi?
Mukandibwezera cilango msanga, mofulumira, ndidzabwezera
cilango canu pamutu panu, 5Popeza inu munatenga siliva wanga
ndi golidi wanga, ndi kulonga zofunika zanga zokoma m'akacisi
anu; 6munagulitsanso ana a Yuda ndi ana a Yerusalemu kwa ana a
Yavani, kuwacotsa kutali kwa malire ao; 7taonani, ndidzawautsa
kumalo kumene munawagulitsako, ndi kubwezera cilango canu
pamutu panu; 8ndipo ndidzagulitsa ana ako amuna ndi akazi
m'dzanja la ana a Yuda; ndipo iwo adzawagulitsa kwa anthu a
Seba, kwa anthu okhala kutari; pakuti Yehova wanena.
9Mulalikire ici mwa amitundu mukonzeretu nkhondo; utsani amuna
amphamvu; amuna onse a nkhondo ayandikire nakwere. 10Sulani
makasu anu akhale malupanga, ndi anangwape anu akhale
nthungo; wofoka anene, Ndine wamphamvu. 11Fulumirani, idzani,
amitundu inu nonse pozungulirapo; sonkhanani pamodzi,
mutsitsire komweko amphamvu anu, Yehova. 12Agalamuke
amitundu, nakwerere ku cigwa ca Yosafati; pakuti ndidzakhala
komweko kuweruza amitundu onse ozungulira, 13Longani zenga,
pakuti dzinthu dzaca; idzani, pondani, pakuti cadzala coponderamo
mphesa; zosungiramo zisefuka; pakuti zoipa zao
nzazikuru. 14Aunyinji, aunyinji m'cigwa cotsirizira mlandu! pakuti
layandikira tsiku la Yehova m'cigwacotsiriziramlandu. 15Dzuwa ndi
mwezi zada, ndi nyenyezi zibweza kuwala kwao. 16Ndipo Yehova
adzadzuma ali ku Ziyoni, ndi kumveketsa mau ace ali ku
Yerusalemu; ndi thambo ndi dziko lapansi zidzagwedezeka; koma
Yehova adzakhala copulumukirako anthu ace, ndi linga la ana a
Israyeli. 17Momwemo mudzadziwa kuti Ine ndine Yehova Mulungu
wanu wakukhala m'Ziyoni, phiri langa lopatulika; pamenepo
Yerusalemu adzakhala wopatulika, osapitanso alendo pakati
pace, 18Ndipo kudzacitika tsiku ilo mapiri adzakhetsa vinyo
wozuna, ndi pazitunda padzayenda mkaka, ndi m'mitsinje yonse
ya Yuda mudzayenda madzi; ndi madzi a kasupe adzaturuka
m'nyumba ya Yehova, nadzamwetsa madzi cigwa ca

Sitimu. 19Aigupto adzasanduka bwinja, ndi Edomu adzasanduka
cipululu copanda kanthu, cifukwa ca ciwawaci anawacitira ana a
Yuda; popeza anakhetsa mwazi wosacimwa m'dziko lao. 20Koma
Yuda adzakhala cikhalire, ndi Yerusalemu ku mibadwo
mibadwo. 21Ndipo ndidzayeretsa mwazi wao umene
sindinauyeretsa, pakuti Yehova akhala m'Ziyoni.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Amos

Amosi 1

Cilango ca Mulungu pa amitundu ozinga Israyeli

1MAU a Amosi, amene anali mwa oweta ng'ombe a ku Tekoa, ndiwo
amene anawaona za Israyeli masiku a Uziya mfumu ya Yuda, ndi
masiku a Yerobiamu mwana wa Yoasi mfumu ya Israyeli, zitatsala
zaka ziwiri cisanafike cibvomezi.
2Ndipo anati, Yehova adzadzuma ali m'Ziyoni, nadzamveketsa mau
ace ali m'Yerusalemu; podyetsa abusa padzacita cisoni, ndi mutu
wa Karimeli udzauma.
3Atero Yehova, Cifukwa ca zolakwa zitatu za Damasiko, kapena
zinai, sindidzabweza kulanga kwace; popeza anapuntha Gileadi ndi
zopunthira zacitsulo; 4koma ndidzatumiza moto ku nyumba ya
Hazaeli, ndipo udzanyeketsa nyumba zacifumu za
Benihadadi. 5Ndipo ndidzatyola mpiringidzo wa Damasiko, ndi
kulikha okhala m'cigwa ca Aveni, ndi iye wogwira ndodo yacifumu
m'Betedeni; ndi anthu a Aramu adzalowa ndende ku Kiri, ati
Yehova.
6Atero Yehova, Cifukwa ca zolakwa zitatu za Gaza, kapena zinai,
sindidzabweza kulanga kwace; popeza anatenga ndende anthu
onse kuwapereka kwa Edomu; 7koma ndidzatumiza moto pa linga
la Gaza, ndipo udzatha nyumba zace zacifumu; 8ndipo ndidzalikha
okhala m'Asidodi, ndi iye wogwira ndodo yacifumu m'Asikeloni;
ndipo ndidzabwezera Ekroni dzanja langa limlange; ndi Afilisti
otsala adzatayika, ati Ambuye Yehova.
9Atero Yehova, Cifukwa ca zolakwa zitatu za Turo, kapena zinai,
sindidzabweza kulanga kwace; popeza anapereka anthu onse kwa
Edomu, osakumbukila pangano lacibale; 10koma ndidzatumiza
moto pa linga la Turo, ndipo udzanyeketsa nyumba zace zacifumu.
11Atero Yehova, Cifukwa ca zolakwa zitatu za Edomu, kapena zinai,
sindidzabweza kulanga kwace; popeza analondola mphwace ndi
lupanga, nafetsa cifundo cace conse, ndi mkwiyo wace
unang'amba cing'ambire, nasunga mkwiyo wace cisungire; 12koma
ndidzatumiza moto pa Temani, udzanyeketsa nyumba zacifumu za
Bozira.
13Atero Yehova, Cifukwa ca zolakwa zitatu za ana a Amoni, kapena
zinai, sindidzabweza kulanga kwace; popeza anatumbula akazi ali
m'pakati a Gileadi, kuti akuze malire ao; 14koma ndidzayatsa moto
pa linga la Raba, udzanyeketsa nyumba zacifumu zace, ndi
kupfuula tsiku la nkhondo, ndi namondwe, tsiku la
kabvumvulu; 15ndipo mfumu yao idzalowa kundende, iyo ndi
akalonga ace pamodzi, ati Yehova.

©The Bible Society of Malawi, 1992

1Atero Yehova, Cifukwa ca zolakwa zitatu za Moabu, kapena zinai,
sindidzabweza kulanga kwace; popeza anatentha mafupa a mfumu
ya ku Edomu asanduke njereza; 2koma ndidzatumiza moto pa
Moabu, udzanyeketsa nyumba zacifumu za Kerioti; ndipo Moabu
adzafa ndi phokoso, ndi kupfuula, ndi mau a lipenga; 3ndipo
ndidzalikha woweruza pakati pace, ndi kupha akalonga ace onse, ati
Yehova.

Cilango ca Mulungu pa Yuda ndi Israyeli

4Atero Yehova, Cifukwa ca zolakwa zitatu za Yuda, kapena zinai,
sindidzabweza kulanga kwace; popeza akaniza cilamulo ca Yehova,
osasunga malemba ace; ndipo awalakwitsa mabodza ao amene
makolo ao anawatsata; 5koma ndidzatumiza moto pa Yuda,
udzanyeketsa nyumba zacifumu za m'Yerusalemu.
6Atero Yehova, Cifukwa ca zolakwa zitatu za Israyeli, kapena zinai,
sindidzabweza kulanga kwace; popeza agulitsa wolungama ndi
ndalama, ndi wosowa cifukwa ca nsapato; 7ndiwo amene aliralira
pfumbi lapansi liri pamutu pa wosauka, napotoza njira ya wofatsa;
ndipo munthu ndi atate wace amuka kwa namwali yemweyo, kuti
aipse dzina langa loyera; 8nagona pansi pa zopfunda za cikole ku
maguwa a nsembe ali onse, ndi m'nyumba ya Mulungu wao
akumwa vinyo wa iwo olipitsidwa. 9Koma ndinaononga Ine pamaso
pa Aamori, amene msinkhu wao unanga msinkhu wa mikungudza,
nakhala nayo mphamvu ngati thundu; koma ndinaononga zipatso
zao m'mwamba, ndi mizu yao pansi. 10Ndipo ndinakukwezani
kucokera m'dziko la Aigupto, ndi kukutsogolerani zaka makumi
anai m'cipululu, kuti mulandire dziko la Aamori likhale colowa
canu. 11Ndipo ndinaukitsa mwa ana anu aneneri, ndi mwa
anyamata anu Anaziri. Si momwemo, inu ana a Israyeli, ati
Yehova? 12Koma munamwetsa Anaziri vinyo, ndi kulamulira
aneneri ndi kuti, Musamanenera. 13Taonani, ndidzakupsinjani
m'malo mwanu, monga lipsinja gareta lodzala ndi mitolo
fwa. 14Ndipo populumukirapo padzasowera waliwiro, ndi
wamphamvu; sadzalimbikitsa mphamvu yace, ndi ngwazi
siidzapulumutsa moyo wace; 15ndi wokoka uta sadzalimbika, ndi
waliwiro sadzadzipulumutsa; ngakhale woyenda pa akavalo
sadzapulumutsa moyo wace; 16ndi wolimba mtima mwa ngwazi
adzathawa wamarisece tsiku lomwelo, ati Yehova.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Obadiah

Obadiya 1

Zoipa zao ndi kulangidwa kwa Aedomu. Dalo la Israyeli

1MASOMPHENYA a Obadiya. Atero Ambuye Yehova za Edomu:
Tamva mbiri yocokera kwa Yehova, ndi mthenga wotumidwa mwa
amitundu, ndi kuti, Nyamukani, timuukire kumthira
nkhondo. 2Taona, ndakuika wamng'ono mwa amitundu; unyozedwa
kwambiri. 3Kudzikuza kwa mtima wako kwakunyenga, iwe wokhala
m'mapanga a thanthwe, iwe pokhala pako pamwamba, wakunena
m'mtima mwace, Adzanditsitsira pansi ndani? 4Cinkana ukwera
pamwamba peni peni ngati ciombankhanga, cinkana cisanja cako
cisanjika pakati pa nyenyezi, ndidzakutsitsa kumeneko, ati
Yehova. 5Akakudzera akuba, kapena mbala usiku, (Ha!
waonongeka) sadzaba mpaka adzakhuta kodi? Akakudzera
akuchera mphesa sadzasiya khunkha kodi? 6Ha! za Esau
zasanthulidwa; ha! zobisika zace zafunidwa. 7Anthu onse a
akupangana nawe anakuperekeza mpaka pamalire; anthu okhala
ndi mtendere nawe anakunyenga, nakuposa mphamvu; iwo
akudya cakudya cako akuchera msampha pansi pako; mulibe
nzeru mwa iye. 8Ati Yehova, Kodi sindidzaononga tsiku lija anzeru
mwa Edomu, ndi luntha m'phiri la Esau? 9Ndipo amuna anu
amphamvu adzatenga nkhawa, Temani iwe, kuti onse aonongeke
m'phiri la Edomu, ndi kuphedwa. 10Cifukwa ca ciwawa unamcitira
mphwako Yakobo, udzakutidwa ndi manyazi, nudzaonongeka ku
nthawi yonse. 11Tsiku lija unaima padera, tsiku lija alendo anagwira
ndende makamu ace, nalowa m'zipata zace acilendo, nacitira
Yerusalemu maere, iwenso unakhala ngati mmodzi wa
iwowa. 12Koma usapenyerera tsiku la mphwako, tsiku loyesedwa
mlendo iye, nusasekerere ana a Yuda tsiku la kuonongeka kwao,
kapena kuseka cikhakha tsiku lakupsinjika. 13Usalowe m'mudzi wa
anthu anga tsiku la tsoka lao, kapena kupenyerera iwe coipa cao
tsiku la tsoka lao, kapena kuthira manja khamu lao tsiku la tsoka
lao. 14Ndipo usaime pamphambano kuononga opulumuka ace;
kapena kupereka otsala ace tsiku lakupsinjika. 15Pakuti tsiku la
Yehova layandikira amitundu onse; monga unacita iwe, momwemo
adzakucitira; cocita iwe cidzakubwererapamtupako. 16Pakuti
monga munamwa pa phiri langa lopatulika, momwemo amitundu
onse adzamwa kosalekeza; inde adzamwa, nadzameza,
nadzakhala monga ngati sanalipo. 17Koma m'phiri la Ziyoni
mudzakhala opulumuka, ndipo lidzakhala lopatulika; ndi a nyumba
ya Yakobo adzakhala nazo zolowa zao. 18Ndipo nyumba ya Yakobo
idzakhala moto, ndi nyumba ya Yosefe lawi, ndi nyumba ya Esau
ngati ciputu, ndipo adzawatentha pakati pao, ndi kuwapsereza;

ndipo sadzakhalapo otsalira nyumba ya Esau; pakuti Yehova wanena. 19Ndipo akumwela adzakhala nalo phiri la Esau colowa cao; ndi iwo a kucidikha adzakhala nalo dziko la Afilisti; ndipo adzakhala nayo minda ya Efraimu, ndi minda ya Samariya colowa cao; ndi Benjamini adzakhala nalo la Gileadi. 20Ndipo andende a khamu ili la ana a Israyeli, okhala mwa Akanani, adzakhala naco colowa cao mpaka pa Zarefati; ndi andende a ku Yerusalemu okhala m'Sefaradi adzakhala nayo midzi ya kumwela, colowa cao. 21Ndipo apulumutsi adzakwera pa phiri la Ziyoni kuweruza phiri la Esau; ndipo ufumu udzakhala wace wa Yehova.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Jonah

Yona 1

Kuitanidwa kwa Yona, kuthawa kwace, ndi kulangidwa kwace

1NDIPO mau a Yehova anadza kwa Yona mwana wa Amitai, ndi
kuti, 2Nyamuka, pita ku Nineve, mudzi waukuruwo, nulalikire
motsutsana nao; pakuti coipa cao candikwerera pamaso
panga. 3Koma Yona ananyamuka kuti athawire ku Tarisi, kuzemba
Yehova; ndipo anatsikira ku Yopa, napezako combo comuka ku
Tarisi, napereka ndalama zace, natsikira m'menemo, kuti apite nao
ku Tarisi kuzemba Yehova. 4Koma Yehova anautsa cimphepo
cacikuru panyanja, ndipo panali namondwe wamkuru panyanja, ndi
combo cikadasweka. 5Pamenepo amarinyero anacita mantha,
napfuulira yense kwa mlungu wace, naponya m'nyanja akatundu
anali m'combo kucipepuza. Koma Yona adatsikira m'munsi mwa
combo, nagona tulo tofa nato. 6Ndipo mwini combo anadza kwa
iye, nanena naye, Utani iwe wam'tulo? uka, itana Mulungu wako,
kapena Mulunguyo adzatikumbukila tingatayike. 7Ndipo anati
yense kwa mnzace, Tiyeni ticite maere, kuti tidziwe coipa ici
catigwera cifukwa ca yani. M'mwemo anacita maere, ndipo maere
anagwera Yona. 8Pamenepo anati kwa iye, Utiuzetu coipa ici
catigwera cifukwa ca yani? nchito yako njotani? ufuma kuti? dziko
lako nliti? nanga mtundu wako? 9Ndipo ananena nao, Ndine
Mhebri, ndiopa Yehova Mulungu wa Kumwamba amene analenga
nyanja ndi mtunda. 10Pamenepo amunawo anaopa kwambiri, nati
kwa iye, Ici nciani wacicita? Pakuti amunawo anadziwa kuti
anathawa pamaso pa Yehova, popeza adawauza. 11Tsono anati kwa
iye, Ticitenji nawe, kuti nyanja iticitire bata? popeza namondwe
anakula-kulabe panyanja. 12Ndipo anati nao, Mundinyamule ndi
kundiponya m'nyanja, momwemo nyanja idzacitira inu bata; pakuti
ndidziwa kuti namondwe wamkuru amene wakugwerani cifukwa ca
ine. 13Koma amunawo anapalasa kubwerera kumtunda, koma
sanathe; pakuti namondwe wa panyanja anakulakula mokomana
nao. 14Pamenepo anapfuulira kwa Yehova, nati, Tikupemphanitu,
Yehova, tisatayike cifukwa ca moyo wa munthu uyu,
musatisenzetse mwazi wosacimwa; pakuti, Inu Yehova, mwacita
monga mudakomera Inu. 15Momwemo ananyamula Yona,
namponya m'nyanja; ndipo nyanja inaleka kukokoma
kwace. 16Ndipo amunawo anaopa Yehova ndi manthaakuru,
namphera Yehova nsembe, nawinda. 17Koma Yehova anaikiratu
cinsomba cacikuru cimeze Yona; ndipo Yona anali m'miroba mwa
nsombayi masiku atatu usana ndi usiku.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Pemphero la Yona ali m'mimba mwa cinsomba

1Pamenepo Yona anapemphera kwa Yehova Mulungu wace ali
m'mimba mwa nsombayo. 2Ndipo anati,
Ndinaitana Yehova m'nsautso yanga,
Ndipo anandiyankha ine;
Ndinapfuula ndiri m'mimba ya manda,
Ndipo munamva mau anga.
3Pakuti munandiponya mwakuya m'kati mwa nyanja,
Ndipo madzi anandizinga;
Mapfunde anu onse a nyondonyondo anandimiza.
4Ndipo ndinati, Ndatayika ndicoke pamaso panu;
Koma ndidzapenyanso Kacisi wanu wopatulika.
5Madzi anandizinga mpaka moyo wanga,
Madzi akuya anandizungulira,
Kayandeyande wa m'nyanja anandikulunga mutu.
6Ndinatsikira ku matsinde a mapiri,
Mipingiridzo ya dziko inanditsekereza kosatha;
Koma munandikwezera moyo wanga kuucotsa kucionongeko,
Yehova Mulungu wanga.
7Pokomoka moyo wanga m'kati mwanga ndinakumbukila Yehova;
Ndi pemphero langa linafikira Inu m'Kacisi wanu wopatulika.
8Iwo osamalira mabodza opanda pace
Ataya cifundo cao cao.
9Koma ine ndidzakupherani Inu nsembe ndi mau akuyamika,
Ndidzakwaniritsacowindacanga.
Cipulumutso nca Yehova.
10Pamenepo Yehova analankhula ndi nsombayo, ndipo inamsanzira
Yona kumtunda.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Yona ku Nineve, Kulapa kwa a ku Nineve

1Ndipo mau a Yehova anadza kwa Yona nthawi yaciwiri, ndi
kuti, 2Nyamuka, pita ku Nineve mudzi waukuru uja, nuulalikire
uthenga umene ndikuuza. 3Ndipo Yona ananyamuka, napita ku
Nineve, monga mwa mau a Yehova. Koma Nineve ndiwo mudzi
waukuru pamaso pa Yehova, wa ulendo wa masiku atatu. 4Ndipo
Yona anayamba kulowa mudziwo ulendo wa tsiku limodzi,
nalalikira, nati, Atsala masiku makumi anai ndipo Nineve
adzapasuka. 5Ndipo anthu a Nineve anakhulupirira Mulungu,
nalalikira cosala, nabvala ciguduli, kuyambira wamkuru kufikira
wamng'ono wa iwowa. 6Pakuti mau awa anafikira mfumu ya
Nineve, ndipo Inanyamuka ku mpando wace wacifumu, nibvula
copfunda cace, nipfunda ciguduli, nikhala m'mapulusa. 7Ndipo
analalikira, nanena m'Nineve mwa lamulo la mfumu ndi nduna
zace, ndi kuti, Ngakhale munthu kapena nyama, ngakhale
ng'ombe kapena nkhosa, zisalawe kanthu, zisadye, zisamwe
madzi; 8koma zipfundidwe ndi ciguduli munthu ndi nyama,
nizipfuulire kolimba kwa Mulungu; ndipo abwere yense kuleka njira
yace yoipa, ndi ciwawa ciri m'manja mwace. 9Kaya, akatembenuka
Mulungu, ndi kuleka kubwera ku mkwiyo wace waukali, kuti
tisatayike, 10Ndipo Mulungu anaona nchito zao, kuti anabwera
kuleka njira yao yoipa; ndipo Mulungu analeka coipa adanenaci
kuti adzawacitira, osacicita.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Kudandaula kwa Yona, kumdzudzula kwa Mulungu

1Koma sikudakomera Yona konse, ndipo anapsa mtima. 2Ndipo
anapemphera kwa Yehova, nati, Ha, Yehova! si ndiwo mau anga
ndikali m'dziko langa? cifukwa cace ndinafulumira kuthawira ku
Tarisi, pakuti ndinadziwa kuti Inu ndinu Mulungu wacisomo ndi
wodzala cifundo, wolekerera ndi wokoma mtima mocuruka, ndi
woleka coipaco. 3Ndipo tsopano, Yehova, mundicotseretu moyo
wanga, kundikomera ine kufa, osakhala ndi moyo ai. 4Ndipo
Yehova anati, Uyenera kupsa mtima kodi? 5Pamenepo Yona
anaturuka m'mudzi, nakhala pansi kum'mawa kwa mudzi,
nadzimangira komweko thandala, nakhala pansi pace mumthunzi
mpaka adzaona cocitikira mudzi. 6Ndipo Yehova Mulungu
anaikiratu msatsi, naumeretsera Yona, ucite mthunzi pamutu pace,
kumlanditsa m'nsautso yace. Ndipo Yona anakondwera kwambiri
cifukwa ca msatsiwo. 7Koma Mulungu anauikira mphanzi pakuca
m'mawa mwace, ndiyo inadya msatsi, nufota. 8Ndipo kunali,
poturuka dzuwa Mulungu anaika mphepo ya kum'mawa yotentha,
ndipo dzuwa linatentha mutu wace wa Yona, nalefuka iye,
nadzipempherera kuti afe; nati, Kundikomera ine kufa, kukhala ndi
moyo ai. 9Ndipo Mulungu anati kwa Yona, Uyenera kodi kupsa
mtima cifukwa ca msatsiwo? Nati iye, Ee, kundiyenera ine kupsa
mtima mpaka imfa. 10Ndipo Yehova anati, Unacitira cifundo
msatsiwo umene sunagwirapo nchito, kapena kuumeretsa, umene
unamera usiku, nutha usiku; 11ndipo sindiyenera Ine kodi kucitira
cifundo Nineve mudzi waukuru uwu; m'mene muli anthu oposa
zikwi zana limodzi mphambu zikwi makumi awiri osadziwa
kusiyanitsa pakati pa dzanja lao lamanja ndi lamanzere, ndi zoweta
zambiri zomwe?

©The Bible Society of Malawi, 1992

Micah

Mika 1

Mau akucenjeza Israyeli ndi Yuda cifukwa ca macimo ao

1MAU a Yehova amene anadza kwa Mika wa ku Morese masiku a
Yotamu, Ahazi, ndi Hezekiya, amene adaona za Samariya ndi
Yerusalemu.
2Imvani, mitundu ya anthu, inu nonse; tamvera, dziko lapansi, ndi
zonse ziri m'mwemo; ndipo Ambuye Yehova akhale mboni
yakutsutsa inu, Ambuye m'Kacisi wace wopatulika. 3Pakuti,
taonani, Yehova alikuturuka m'malo mwace, nadzatsika,
nadzaponda pa misanje ya dziko lapansi. 4Ndi mapiri
adzasungunuka pansi pa Iye, ndi zigwa zidzang'ambika, ngati sera
pamoto, ngati madzi otsanulidwa potsetseremba. 5Cicitika ici
conse cifukwa ca kulakwa kwa Yakobo, ndi macimo a nyumba ya
Israyeli. Kulakwa kwa Yakobo nkotani? Si ndiko Samariya? ndi
misanje ya Yuda ndi iti? si ndiyo Yerusalemu? 6Cifukwa cace
ndidzaika Samariya ngati mulu wa miyala ya m'munda, ngati
zooka m'munda wamphesa; ndipo ndidzataya miyala yace
m'cigwa, ndi kufukula maziko ace. 7Ndi mafano ace osema onse
adzaphwanyika, ndi mphotho zace zonse zidzatenthedwa ndi
moto, ndi mafano ace onse ndidzawapasula; pakuti
anazisonkhanitsa pa mphotho ya mkazi waciwerewere, ndipo
zidzabwerera ku mphotho ya mkazi waciwerewere. 8Cifukwa ca ici
ndidzacita maliro, ndi kucema, ndidzayenda wolandidwa ndi
wamarisece; ndidzalira ngati mimbulu, ndi kubuma ngati
nthiwatiwa. 9Pakuti mabala ace ndi osapola; pakuti afikira ku Yuda;
afikira ku cipata ca anthu anga, ku Yerusalemu. 10Musacifotokoza
m'Gati, musalira misozi konse; m'nyumba ya Afira ndinagubuduka
m'pfumbi. 11Pitiratu, wokhala m'Safiri iwe, wamarisece ndi
wamanyazi; wokhala m'Zanana sanaturuka; maliro a Betezeli
adzakulandani pokhala pace. 12Pakuti wokhala m'Maroti alindira
cokoma, popeza coipa catsika kwa Yehova kumka ku cipata ca
Yerusalemu. 13Manga gareta ku kavalo waliwiro, wokhala m'Lakisi
iwe, woyamba kucimwitsa mwana wamkazi wa Ziyoni ndi iye;
pakuti zolakwa za Israyeli zinapezedwa mwa iwe. 14Cifukwa cace
pereka mphatso zolawirana kwa Moreseti Gati; nyumba za Akizibi
zidzakhala cinthu cabodza kwa mafumu a
Israyeli. 15Ndidzakutengeranso wokhala m'Maresa iwe, iye amene
adzakulandira ukhale colowa cace; ulemerero wa Israyeli udzafikira
ku Adulamu. 16Udziyeseze wadazi, udzimete wekha cifukwa ca ana
ako okondwera nao; kuza dazi lako ngati la muimba; pakuti
anakucokera, nalowa ndende.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Mau akutsutsa akulanda za eni

1Tsoka iwo akulingirira cinyengo, ndi kukonza coipa pakama pao!
kutaca m'mawa acicita, popeza cikhozeka m'manja mwao. 2Ndipo
akhumbira minda, nailanda; ngakhale nyumba, nazicotsa; asautsa
mwamuna ndi nyumba yace, inde munthu ndi colowa
cace. 3Cifukwa cace atero Yehova, Taonani, ndilingirira coipa pa
banja ili, cimene simudzacotsako makosi anu, kapena kuyenda
modzikuza inu; Pakuti nyengo iyi ndi yoipa. 4Tsiku ilo adzanena
fanizo lakunena inu, nadzalira maliro olemerera, ndi kuti, Tapasuka
konse; iye asintha gawo la anthu anga; ha! andicotsera ili! agawira
opikisana minda yathu. 5Cifukwa cace udzasowa woponya cingwe
camaere m'msonkhano wa Yehova. 6Musamanenera, amanenera
ati. Sadzanenera kwa awa; matonzo sadzacoka. 7Kodi adzati,
Nyumba ya Yakobo iwe, Mzimu wa Yehova waperewera kodi? izi ndi
nchito zace kodi? Mau anga samcitira zokoma kodi, iye amene
ayenda coongoka? 8Koma ngakhale dzulo anthu anga anauka ngati
mdani; mukwatula copfunda ku maraya a iwo opitirira
mosatekeseka, ngati anthu osafuna nkhondo. 9Muwataya akazi a
anthu anga kunja kwa nyumba zao zokondweretsa; mucotsa
ulemerero wanga kwa ana ao kosatha. 10Nyamukani, cokani,
pakuti popumula panu si pano ai; cifukwa ca udio Wakuononga ndi
cionongeko cacikuru. 11Munthu akayenda ndi mtima wacinyengo
ndi kunama, ndi kuti, Ndidzanenera kwa iwe za vinyo ndi cakumwa
cakuledzeretsa; iye ndiye mneneri wa anthu ace.
12Ndidzakumemezani ndithu, Yakobo, inu nonse;
ndidzasonkhanitsa ndithu otsala a Israyeli; ndidzawaika pamodzi
ngati nkhosa za ku Boma; ngati zoweta pakati pa busa pao
adzacita phokoso cifukwa ca kucuruka anthu. 13Wotyola wakwera
pamaso pao; iwo anatyola, napita kucipata, naturuka pomwepo;
ndi mfumu yao yapita pamaso pao, ndipo Yehova awatsogolera.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Cilangizo ca Mulungu cifukwa ca atsogoleri ndi aneneri onyenga

1Ndipo ndinati, Imvanitu, inu akuru a Yakobo, ndi oweruza a
nyumba ya Israyeli; simuyenera kodi kudziwa ciweruzo? 2inu
amene mudana naco cokoma ndi kukondana naco coipa; inu
akumyula khungu lao pathupi pao, ndi mnofu wao pa mafupa
ao; 3inu amene mukudyanso mnofu wa anthu anga; ndi kusenda
khungu lao ndi kutyola mafupa ao; inde awaduladula ngati nyama
yoti aphike, ndi ngati nyama ya mumphika. 4Pamenepo
adzapfuulira kwa Yehova, koma sadzawayankha; inde,
adzawabisira nkhope yace nthawi yomweyo, monga momwe
anaipsa macitidwe ao. 5Atero Yehova za aneneriakulakwitsa anthu
anga; akuluma ndi mano ao, ndi kupfuula, Mtendere; ndipo, ali
yense wosapereka m'kamwa mwao, amkonzera nkhondo; 6cifukwa
cace kudzakhala ngati usiku kwa inu, wopanda masomphenya;
ndipo kudzadera inu, wopanda kulosa; ndi dzuwa lidzalowera
aneneri, ndi usana udzawadera bii. 7Ndipo alauli adzacita manyazi,
ndi olosa adzathedwa nzeru; ndipo onsewo adzasunama; pakuti
kuyankha kwa Mulungu kulibe. 8Koma ine ndidzala nayo mphamvu
mwa Mzimu ya Yehova, ndi ciweruzo, ndi camuna, kufotokozera
Yakobo kulakwa kwace, ndi kwa Israyeli cimo lace. 9Tamvanitu ici,
akuru a nyumba ya Yakobo inu, ndi oweruza a nyumba ya Israyeli
inu, akuipidwa naco ciweruzo, ndi kupotoza zoongoka
zonse. 10Amanga Ziyoni ndi mwazi, ndi Yerusalemu ndi
cisalungamo. 11Akuru ace aweruza cifukwa ca mphotho, ndi
ansembe ace aphunzitsa cifukwa ca malipo, ndi aneneri ace alosa
cifukwa ca ndarama; koma atsamira pa Yehova, nati, Kodi Yehova
sali pakati pa ife? palibe coipa codzatigwera. 12Momwemo Ziyoni
adzalimidwa ngati: munda cifukwa ca inu, ndi m'Yerusalemu
mudzasanduka miunda, ndi phiri la nyumba ngati misanje ya
m'nkhalango.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Kuitanidwa kwa amitundu

1Koma kudzacitika masiku otsiriza, kuti phiri la nyumba ya Yehova
lidzakhazikika pamwamba pa mapiri, nilidzakuzika pamwamba pa zitunda; ndi
mitundu ya anthu idzayendako. 2Ndipo amitundu ambiri adzamuka, nadzati,
Tiyeni, tikwere ku phiri la Yehova, ndi ku nyumba ya Mulungu wa Yakobo; kuti
Iye atiphunzitse njira zace, ndipo tidzayenda m'mabande ace; pakuti ku Ziyoni
kudzaturuka cilamulo, ndi ku Yerusalemu mau a Yehova. 3Ndipo Iye
adzaweruza mwa mitundu yambiri ya anthu, nadzadzudzula amitundu
amphamvu ali kutali; ndipo iwo adzasula malupanga ao akhale makasu, ndi
mikondo yao ikhale mazenga, mtundu wa anthu sudzasamulira mtundu
unzace lupanga, kapena kuphunziranso nkhondo. 4Koma adzakhala munthu
yense patsinde pa mpesa wace, ndi patsinde pa mkuyu wace; ndipo
sipadzakhala wakuwaopsa; pakuti pakamwa pa Yehova wa makamu
padanena. 5Pakuti mitundu yonse ya anthu idzayenda, wonse m'dzina la
mlungu wace, ndipo ife tidzayenda m'dzina la Yehova Mulungu wathu ku
nthawi yomka muyaya.
6Tsiku ilo, ati Yehova, ndidzamemeza wakutsimphinayo, ndi kusonkhanitsa
wopitikitsidwayo, ndi iye amene ndinamsautsa; 7ndipo wotsimphinayo
ndidzamuyesa wotsala, ndi iye wotayidwa kutali mtundu wamphamvu; ndipo
Yehova adzakhala mfumu yao m'phiri la Ziyoni kuyambira pamenepo kufikira
kosatha. 8Ndipo iwe, nsanja ya nkhosa, citunda ca mwana wamkazi wa Ziyoni,
udzafikira iwe, inde udzafika ulamuliro wakale, ufumu wa mwana wamkazi wa
Yerusalemu. 9Tsono upfuulitsa cifukwa ninji? palibe mfumu mwa iwe kodi?
watayika kodi mu uphungu wako, kuti zowawa zakugwira ngati mkazi
wobala? 10Imva zowawa, nuyesetse kubala, mwana wamkazi wa Ziyoni, ngati
mkazi wakubala; pakuti udzaturuka m'mudzi tsopano, nudzakhala kuthengo,
nudzafika ku Babulo; komweko udzapulumutsidwa; komweko Yehova
adzakuombola m'manja a adani ako. 11Ndipo tsopano amitundu ambiri
asonkhana kuyambana nawe, akuti, Aipsidwe, diso lathu lipenye ku
Ziyoni. 12Koma sadziwa zolingirira za Yehova, kapena kuzindikira uphungu
wace; pakuti anawasonkhanitsa ngati mitolo kudwale. 13Nyamuka nupunthe,
mwana wamkazi wa Ziyoni; pakuti ndidzasanduliza nyanga yako ikhale
yacitsulo, ndi ziboda zako zikhale zamkuwa; ndipo udzaphwanya mitundu
yambiri ya anthu; ndipo uzipereka ciperekere phindu lao kwa Yehova, ndi
cuma cao kwa Ambuye wa dziko lonse lapansi.

1Uzisonkhana tsopano magulu magulu, mwana wamkazi wa magulu
iwe; watimangira misasa, adzapanda woweruza wa Israyeli ndi
ndodo patsaya.
Aneneratu za kubadwa kwa woweruza m'Israyeli
2Koma iwe, Betelehemu Efrata, ndiwe wamng'ono kuti ukhale mwa
zikwi za Yuda, mwa iwe mudzanditurukira wina wakudzakhala
woweruza m'Israyeli; maturukiro ace ndiwo a kale lomwe,
kuyambira nthawi yosayamba. 3Cifukwa cace Iye adzawapereka
kufikira nthawi yoti wobalayo wabala; pamenepo otsala a abale
ace adzabwera pamodzi ndi ana a Israyeli, 4Ndipo adzaimirira,
nadzadyetsa nkhosa zace mu mphamvu ya Yehova, m'ukulu wa
dzina la Yehova Mulungu wace; ndipo iwo adzakhalabe; pakuti
pamenepo Iye adzakhala wamkuru kufikira malekezero a dziko
lapansi. 5Ndipo ameneyo adzakhala Mtendere; pamene a ku Asuri
adzalowa m'dziko lathu, ndi pamene adzaponda m'zinyumba
zathu, tidzawaukitsira abusa asanu ndi awiri, ndi akalonga asanu
ndi atatu. 6Ndipo iwo adzatha dziko la Asuri ndi lupanga, ndi dziko
la Nimrodi, ndilo polowera pace; ndipo adzatilanditsa kwa a ku
Asuri pamene alowa m'dziko lathu, pamene aponda m'kati mwa
malire athu. 7Ndipo otsala a Yakobo adzakhala pakati pa mitundu
yambiri ya anthu, ngati mame ocokera kwa Yehova, ngati mvula
paudzu, yosacedwera munthu, yosalindira ana a anthu. 8Ndipo,
otsala a Yakobo adzakhala mwa amitundu, pakati pa mitundu
yambiri ya anthu, ngati mkango mwa nyama za kuthengo, ngati
msona wa mkango mwa magulu a nkhosa; umenewo ukapitako,
upondereza, numwetula, ndipo palibe wakupulumutsa. 9Dzanja
lako likwezeke pamwamba pa iwo akuyambana nawe, ndi adani
ako onse aonongeke.
10Ndipo kudzacitika tsiku ilo, ati Yehova, ndidzaononga akavalo ako
m'kati mwako, ndi kutha magareta ako; 11ndipo ndidzaononga
midzi ya m'dziko lako, ndi kupasula malinga ako onse; 12ndipo
ndidzaononga zanyanga za m'dzanja lako; ndipo sudzakhalanso
nao alosi; 13ndidzaononganso mafano ako osema, ndi zoimiritsa
zako pakati pako; ndipo sudzalambiranso nchito za manja
ako. 14Ndipo ndidzazula zifanizo zako m'kati mwako, ndi kutha
midzi yako. 15Ndipo ndidzabwezera amitundu osamvera cilango
mu mkwiyo waukali.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Mulungu atsutsana ndi anthu ace cifukwa ca zoipa zao

1Tamverani tsono conena Yehova: Nyamuka, tsutsana nao mapiri,
ndi zitunda zimve mau ako. 2Tamvani, mapiri inu, citsutsano ca
Yehova, ndi inu maziko olimba a dziko lapansi; pakuti Yehova ali
naco citsutsano ndi anthu ace, ndipo adzatsutsana ndi
Israyeli. 3Anthu anga inu, ndakucitirani ciani? ndakulemetsani ndi
ciani? citani umboni wonditsutsa. 4Pakuti ndinakukwezani
kukuturutsani m'dziko la Aigupto, ndi kuombola inu m'nyumba ya
ukapolo; ndipo ndinatuma akutsogolereni Mose, Aroni, ndi
Miriamu. 5Anthu anga, kumbukilanitu cofunsira Balaki mfumu ya
Moabu, ndi comuyankha Balamu mwana wa Beori, kuyambira ku
Sitimu kufikira ku Giligala; kuti mudziwe zolungama za
Yehova. 6Ndidzafika kwa Yehova ndi ciani, ndi kuwerama kwa
Mulungu Wam'mwamba? Kodi ndifike kwa Iye ndi nsembe
zopsereza, ndi ana a ng'ombe a caka cimodzi? 7Kodi Yehova
adzakondwera nazo nkhosa zamphongo zikwi, kapena ndi mitsinje
ya mafuta zikwi khumi? Kodi ndipereke mwana wanga woyamba
cifukwa ca kulakwa kwanga, cipatso ca thupi langa cifukwa ca
kucimwa kwa moyo wanga? 8Iye anakuuza, munthuwe, comwe ciri
cokoma; ndipo Yehova afunanji nawe koma kuti ucite colungama,
ndi kukonda cifundo ndi kuyenda modzicepetsa ndi Mulungu wako?
9Mau a Yehova aitana mudzi, ndi wanzeru aopa dzina lanu;
tamverani ndodo, ndi Iye amene anaiika. 10Kodi m'nyumba ya
woipa mukali cuma cosalungama, ndi muyeso wocepa umene
ayenera kuipidwa nao? 11Kodi ndikhoza kuyera ndi miyeso yoipa,
ndi thumba la miyala yonyenga? 12Pakuti anthu ace olemera
adzala ndi ciwawa, ndi okhalamo amanena bodza, ndi lilime lao
limacita monyenga m'kamwa mwao. 13Cifukwa cace Inenso
ndakukantha ndi kukupweteketsa; ndakupulula cifukwa ca
zocimwa zako. 14Udzadya koma osakhuta; ndi njala yako idzakhala
pakati pako; ndipo udzacotsa koma osalanditsa; ndi ici
wacilanditsa ndidzacipereka kulupanga. 15Udzafesa koma osaceka;
udzaponda azitona koma osadzola mafuta; udzaponda mphesa
koma osamwa vinyo. 16Pakuti asunga malemba a Omri, ndi nchito
za nyumba ya Ahabu, ndipo mumayenda m'uphungu wao; kuti
ndikusandulize bwinja, ndi okhalamo cotsonya; ndipo mudzasenza
citonzo ca anthu anga.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Za kuipa kwakukuru kwa Aisrayeli, ndi cifundoca Mulungu

1Kalanga ine! pakuti ndikunga atapulula zipatso za m'mwamvu,
atakunkha m'munda wamphesa; palibe mphesa zakudya; moyo
wanga ukhumba nkhuyu yoyamba kupsa. 2Watha wacifundo
m'dziko, palibe woongoka mwa anthu; onsewo alalira mwazi;
yense asaka mbale wace ndi ukonde. 3Manja ao onse awiri agwira
coipa kucicita ndi cangu; kalonga apempha, ndi woweruza aweruza
cifukwa ca mphotho; ndi wamkuruyo angonena cosakaza moyo
wace; ndipo aciluka pamodzi. 4Wokoma wa iwo akunga mitungwi;
woongoka wao aipa koposa mpanda waminga; tsiku la alonda ako
la kulangidwa kwako lafika, tsopano kwafika kuthedwa nzeru
kwao. 5Musakhulupirira bwenzi, musatama bwenzi loyanja;
usamtsegulire pakhomo pakamwa pako, ngakhale kwa iye wogona
m'fukato mwako. 6Pakuti mwana wamwamuna apeputsa atate,
mwana wamkazi aukira amace, mpongozi aukira mpongozi wace;
adani ace a munthu ndiwo a m'nyumba yace.
7Koma ine, ndidzadikira Yehova; ndidzalindirira Mulungu wa
cipulumutso canga; Mulungu wanga adzandimvera. 8Usandiseka,
mdani wangawe; pakugwa ine ndidzaukanso; pokhala ine
mumdima Yehova adzakhala kuunika kwanga. 9Ndidzasenza
mkwiyo wa Yehova, cifukwa ndamcimwira, mpaka andinenera
mlandu wanga, ndi kundiweruzira mlandu wanga; adzanditurutsira
kwa kuunika, ndipo ndidzapenya cilungamo cace. 10Pamenepo
mdani wanga adzaciona, ndi manyazi adzamkuta iye amene adati
kwa ine, Ali kuti Yehova Mulungu wako? Maso anga adzamuona;
tsopano adzampondereza ngati thope la m'miseu. 11Tsiku
lakumanga malinga ako, tsiku lomwelo lembalo lidzacotsedwa
kunka kutali. 12Tsiku lomwelo adzadza kwa iwe, kucokera ku Asuri
ndi midzi ya ku Aigupto, kuyambira ku Aigupto kufikira ku Mtsinje,
ndi kuyambira kunyanja kufikira kunyanja, ndi kuyambira kuphiri
kufikira kuphiri. 13Koma dziko lidzakhala labwinja cifukwa ca iwo
okhalamo, mwa zipatso za macitidwe ao.
14Mudyetse anthu anu ndi ndodo yanu, nkhosa za colowa canu
zokhala pa zokha m'nkhalango pakati pa Karimeli, zidye m'Basana
ndi m'Gileadi masiku a kale lomwe. 15Monga masiku a kuturuka
kwako m'dziko la Aigupto ndidzamuonetsa zodabwitsa. 16Amitundu
adzaona nadzacita manyazi ndi mphamvu yao yonse; adzagwira
pakamwa, m'makutu mwao mudzagontha. 17Adzanyambita pfumbi
ngati njoka; ngati zokwawa za padziko, adzanjenjemera poturuka
m'ngaka mwao; adzafika kwa Yehova Mulungu wao ndi mantha,
nadzaopa cifukwa ca iwe. 18Ndani Mulungu wofanana ndi Inu,
wakukhululukira mphulupulu, wakupitirira zolakwa za otsala a
colowa cace? sasunga mkwiyo wace ku nthawi yonse popeza

akondwera naco cifundo. 19Adzabwera, nadzaticitira nsoni;
adzagonjetsa mphulupulu zathu; ndipo mudzataya zocimwa zao
zonse m'nyanja yakuya, 20Mudzapatsa kwa Yakobo coonadi, ndi
kwa Abrahamu cifundo cimene munalumbirira makolo athu
kuyambira masiku a kale lomwe.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Nahum

Nahumu 1

Cilungamo ndi cifundo ca Mulungu. Adzaononga adani ndi kulanditsa anthu ace

1KATUNDU wa Nineve. Buku la masomphenya a Nahumu wa ku
Elikosi.
2Yehova ndiye Mulungu wansanje, nabwezera cilango; Yehova
ndiye wobwezera cilango, ndi waukali ndithu; Yehova ndiye
wobwezera cilango oyambana naye, nasungira mkwiyo pa adani
ace. 3Yehova ndiye wolekerera mkwiyo, koma wa mphamvu
yaikuru; ndi wosamasula ndithu woparamula; njira ya Yehova iri
m'kabvumvulu ndi mumkuntho; ndipo mitambo ndiyo pfumbi la
mapazi ace. 4Adzudzula nyanja, naiphwetsa, naumitsa mitsinje
yonse; Basana ndi Karimeli afota, ndi duwa la ku Lebano
linyala. 5Mapiri agwedezeka cifukwa ca Iye, ndi zitunda
zisungunuka; ndi dziko lapansi likwezeka pamaso pace, ndi maiko
ndi onse okhala m'mwemo. 6Adzaima ndani pa kulunda kwace?
ndipo adzakhalitsa ndani pa mkwiyo wace wotentha? ukali wace
utsanulidwa ngati moto, ndi matanthwe asweka ndi Iye. 7Yehova
ali wabwino, ndiye polimbikirapo tsiku la msauko; ndipo adziwa iwo
omkhulupirira Iye. 8Koma ndi cigumula cosefukira adzatha konse
malo ace, nadzapitikitsira adani ace kumdima. 9Mulingaliranji
cotsutsana ndi Yehova? Iye adzatha psiti; nsautso siidzauka
kawiri. 10Pakuti cinkana akunga minga yoyangayanga, naledzera
naco coledzeretsa cao, adzathedwa konse ngati ciputu
couma. 11Mwa iwe waturuka wina wolingalira coipa cotsutsana ndi
Yehova, ndiye phungu wopanda pace. 12Atero Yehova: Angakhale
iwo ali ndi mphamvu yokwanira, nacuruka momwemo, koma
momwemonso adzasalikidwa, ndipo iye adzapitiratu. Cinkana
ndakuzunza iwe, sindidzakuzunzanso. 13Koma tsopano ndidzatyola
ndi kukucotsera goli lace, ndipo ndidzadula zomangira
zako. 14Ndipo Yehova walamulira za iwe kuti asabzalidwenso ena a
dzina lako; m'nyumba ya milungu yako ndidzacotsa fano losema
ndi fano loyenga; ndidzakukonzerapo manda, pakuti iwe ndiwe
wopepuka. 15Taonani pamapiri mapazi a iye wakulalikira uthenga
wabwino, wakubukitsa mtendere! cita madyerero ako, Yuda,
kwaniritsa zowinda zako; pakuti wopanda paceyo sadzapitanso
mwa iwe; iye waonongeka konse.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Nineve amangidwa misasa nalandidwa

1Wophwanyayo wakwera pamaso pako; sunga linga, yang'anira panjira,
limbitsa m'cuuno mwako, limbikitsatu mphamvu yako. 2Pakuti Yehova
abwezeranso ukulu wace wa Yakobo ngati ukulu wace wa Israyeli; pakuti
okhuthula anawakhuthula, naipsa nthambi zace za mpesa. 3Zikopa za
amphamvu ace zasanduka zofiira, ngwazi zibvala mlangali; magareta
anyezimira ndi citsulo tsiku la kukonzera kwace, ndi mikondo
itinthidwa. 4Magareta acita mkokomo m'miseu, akankhana m'makwalala;
maonekedwe ao akunga miuni, athamanga ngati mphezi. 5Akumbukila
omveka ace; akhumudwa m'kupita kwao, afulumira ku linga lace, ndi
cocinjiriza cakonzeka. 6Pa zipata za mitsinje patseguka, ndi cinyumba
casungunuka. 7Catsimikizika, abvulidwa, atengedwa, adzakazi ace alira ngati
mau a nkhunda, nadziguguda pacifuwa pao. 8Koma Nineve wakhala ciyambire
cace ngati thamanda lamadzi; koma athawa. Imani, Imani! ati, koma palibe
woceuka. 9Funkhani siliva, funkhani golidi; pakuti palibe kutha kwace kwa
zosungikazo, kwa cuma ca zipangizo zofunika ziri zonse. 10Ndiye mopanda
kanthu mwacemo ndi mwacabe, ndi wopasuka; ndi mtima usungunuka, ndi
maondo aombana, ndi m'zuuno zonse muwawa, ndi nkhope zao
zatumbuluka. 11Iri kuti ngaka ya mikango, ndi podyera misona ya mikango;
kumene mkango, waumuna ndi waukazi, ukayenda ndi mwana wa mkango,
kopanda wakuiposa? 12Mkangowo unamwetula zofikira ana ace, nusamira
yaikazi yace, nudzaza mapanga ace ndi nyama, ngaka zace ndi
zojiwa. 13Taona, nditsutsana nawe, ati Yehova wa makamu, ndipo
ndidzatentha magareta ace m'utsi; ndi lupanga lidzadya misona yako ya
mkango; ndipo ndidzacotsa zofunkha zako pa dziko lapansi, ndi mau a
mithenga yako sadzamvekanso.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Zoipa za Nineve ndi kupasuka kwace

1Tsoka mudzi wa mwazi! udzala nao mabodza ndi zacifwamba;
zacifwamba sizidukiza. 2Kumveka kwa cikoti, ndi mkokomo wa
kuyenda kwa njinga za magareta; ndi kaphata kaphata wa akavalo,
ndi gwegwegwe wa magareta; 3munthu wokwera pa kavalo, ndi
lupanga lonyezimira, ndi mkondo wong'anipa; ndi aunyinji
ophedwa, ndi cimulu ca mitembo, palibe kutha zitanda;
angokhumudwa ndi zitanda; 4cifukwa ca ciwerewere cocuruka ca
waciwerewere wokongola, ndiye mkaziyo mwini nyanga,
wakugulitsa amitundu mwa ciwerewere cace, ndi mabanja mwa
nyanga zace. 5Taona, nditsutsana nawe, ati Yehova wa makamu,
ndidzaphimba nkhope yako ndi nsaru yako yoyesa mthendene;
ndipo ndidzaonetsa amitundu umarisece wako, ndi maufumu
manyazi ako. 6Ndipo ndidzakuponyera zonyansa, ndi kukucititsa
manyazi, ndi kukuika copenyapo, 7Ndipo kudzali kuti onse
akupenyerera iwe adzakuthawa, nadzati, Nineve wapasuka,
adzamlira maliro ndani? ndidzakufunira kuti akukutonthoza? 8Kodi
uli wabwino woposa No-Amoni, wokhala pakati pa mitsinje
wozingidwa ndi madzi; amene chemba lace ndilo nyanja, ndi linga
lace ndilo nyanja? 9Kusi ndi Aigupto ndiwo mphamvu yace, ndiyo
yosatha, Puti ndi Lubimu ndiwo akukuthandiza. 10Koma iye
anatengedwa, analowa ndende; ana ace a makanda anaphwanyika
polekeza pace pa miseu yace yonse; ndi pa omveka ace anacita
maere, ndi akulu ace onse anamangidwa maunyolo. 11Iwenso
udzaledzera, udzabisala; iwenso udzafunanso polimbikira cifukwa
ca mdani. 12Malinga ako onse adzanga mikuyu ndi nkhuyu
zoyamba kupsa; akaigwedeza zingokugwa m'kamwa mwa
wakudya. 13Taona, anthuako m'kati mwako akunga akazi; zipata za
dziko lako zatsegulidwira adani ako papakuru; moto watha
mipingiridzo yako. 14Udzitungiretu madzi a nthawi yokumangira
misasa, limbikitsa malinga ako, lowa kuthope, ponda dothi,
limbitsa ng'anjo yanjerwa. 15Pomwepo moto udzatha iwe; lupanga
lidzakuononga; lidzatha iwe ngati cirimamine; udzicurukitse ngati
cirimamine, udzicurukitse ngati dzombe. 16Wacurukitsa amalonda
ako koposa nyenyezi za kuthambo; cirimamine anyambita,
nauluka, nathawa. 17Obvala korona ako akunga dzombe, ndi
akazembe, ndi akazembe ako ngati ziwalamsatsi zakutera
m'macinga tsiku lacisanu, koma likafundukula dzuwa ziuluka
nizithawa, ndi kumene zinakhalako sikudziwikanso. 18Abusa ako
aodzera, mfumu ya ku Asuri; omveka ako apumula; anthu ako
amwazika pamapiri, ndipo palibe wakuwasonkhanitsa. 19Palibe
cakulunzitsa kutyoka kwako; bala lako liwawa; onse akumva mbiri

yako akuombera manja; pakuti ndaniyo kuipa kwako sikunampitapitabe?

©The Bible Society of Malawi, 1992

Habbakuk

Habakuku 1

Cisalungamo ca Ayuda. Akasidi adzawadzera ndi kuononga zonse. Mneneri apempherera Ayuda

1KATUNDU adamuona Habakuku 2Yehova, ndidzapfuula mpaka liti
osamva Inu? ndipfuulira kwa Inu za ciwawa, koma
simupulumutsa. 3Mundionetseranji zopanda pace, ndi kundionetsa
zobvuta? pakuti kufunkha ndi ciwawa ziri pamaso panga; ndipo pali
ndeli nauka makani. 4Pakuti cilamulo calekeka, ndi ciweruzo
siciturukira konse; popeza woipa azinga wolungama, cifukwa cace
ciweruzo cituruka copindika. 5Penyani mwa amitundu,
penyetsetsani, nimudabwe kwakukuru, pakuti ndicita nchito
masiku anu, imene simudzabvomera cinkana
akufotokozerani. 6Pakuti taonani, ndiukitsa Akasidi, mtundu uja
wowawa ndi waliwiro, wopitira, pa citando ca dziko lapansi, kulowa
m'malo mosati mwao, mukhale mwao mwao. 7Ali oopsa, acititsa
mantha, ciweruzo cao ndi ukulu wao zituruka kwa iwo
eni. 8Akavalo ao aposa anyalugwe liwiro lao, aposa mimbulu ya
madzulo ukali wao, ndipo apakavalo ao atanda; inde apakavalo ao
afumira kutali; auluka ngati ciombankhanga cofulumira
kudya. 9Adzera ciwawa onsewo; nkhope zao zikhazikika zolunjika
m'tsogolo; asonkhanitsa andende ngati mcenga, 10Inde anyoza
mafumu, aseka akalonga; aseka linga liri lonse; popeza aunjika
dothi, nalilanda. 11Pamenepo adzapitirira ngati mphepo,
oadzalakwa ndi kuparamula, iye amene aiyesa mphamvu yace
mulungu wace. 12Si ndinu wacikhalire, Yehova Mulungu wanga,
wopatulika wanga? sitidzafa. Yehova munamuikiratu kuti
aweruzidwe; ndipo Inu, Thanthwe, munamkhazika kuti
alangidwe. 13Inu wa maso osalakwa, osapenya coipa, osakhoza
kupenyerera cobvuta, mupenyereranji iwo akucita mocenjerera,
ndi kukhala cete pamene woipa ammeza munthu wolungama
woposa iye mwini; 14ndi kuyesa anthu ngati nsomba za m'nyanja,
ngati zokwawa zopanda wakuzilamulira. 15Aziwedza zonse ndi
mbedza, azigwira m'ukonde wace, nazisonkhanitsa m'khoka
mwace; cifukwa cace asekera nakondwerera. 16Cifukwa cace
aphera nsembe ukonde wace, nafukizira khoka lace, pakuti mwa izi
gawo lace lilemera, ndi cakudya cace cicuruka. 17Kodi m'mwemo
adzakhuthula m'ukonde mwace osaleka kuphabe amitundu?

©The Bible Society of Malawi, 1992

Akasidi omwe adzalangidwa

1Ndidzaima pa dindiro langa ndi kudziika palinga, ndipo
ndidzayang'anira ndione ngati adzanenanji mwa ine, ngatinso
ndidzamyankha ciani pa coneneza canga. 2Ndipo Yehova
anandiyankha nati, Lembera masomphenyawo, nuwacenutse
pamagome, kuti awawerenge mofulumira. 3Pakuti
masomphenyawo alindira nyengo yoikidwiratu, ndipo afulumirira
potsirizira pace, osanama; akacedwa uwalindirire; popeza afika
ndithu, osazengereza. 4Taonani, moyo wace udzikuza, wosaongoka
m'kati mwace; koma wolungama adzakhala ndi moyo mwa
cikhulupiriro cace. 5Ndiponso vinyo ngwonyenga, ngati munthu
wodzikuza, wosakhala kwao; wakukulitsa cikhumbo cace ngati
kunsi kwa manda, akunga imfa, yosakhuta, koma adzisonkhanitsira
amitundu onse, nadzimemezera mitundu yonse ya anthu. 6Kodi
sadzamnenera fanizo onsewo, ndi mwambi womnyodola, ndi kuti,
Tsoka iye wocurukitsa zimene siziri zace! mpaka liti? iye
wodzisenzera zigwiriro. 7Sadzauka kodi modzidzimuka iwo amene
adzakuluma, ndi kugalamuka iwo amene adzakugwedezetsa; ndipo
udzakhala zofunkha zao? 8Popeza iwe wafunkha amitundu ambiri,
otsala onse a mitundu ya anthu adzakufunkha iwe; cifukwa ca
mwazi wa anthu, ndi ciwawa cocitikira dziko, mudzi, ndi onse
okhalamo.
9Tsoka iye wakupindulitsira nyumba yace phindu loipa, kuti aike
cisanja cace ponyamuka, kuti alanditsidwe m'dzanja la
coipa! 10Wapangira nyumba yako camanyazi, pakuononga mitundu
yambiri ya anthu, ndipo wacimwira moyo wako. 11Pakuti mwala wa
m'khoma upfuula, ndi mtanda wa kuphaso udzaubvomereza.
12Tsoka tye wakumanga mudzindi mwazi, nakhazikitsa mudzi ndi
cisalungamo! 13Taonani, sicicokera kwa Yehova wa makamu kodi
kuti mitundu ya anthu ingogwirira moto nchito, ndi anthu
angodzilemetsa pa zopanda pace? 14Pakuti dziko lapansi
lidzadzazidwa ndi cidziwitso ca ulemerero wa Yehova, monga
madzi aphimba pansi panyanja.
15Tsoka wakuninkha mnzace cakumwa, ndi kuonjezako mankhwala
ako, ndi kumledzeretsa, kuti upenyerere manyazi ao! 16Udzazidwa
nao manyazi m'malo mwa ulemerero; imwa iwenso, nukhale
wosadulidwa; cikho ca dzanja lamanja la Yehova cidzatembenukira
iwe, ndi kusanza kwa manyazi kudzakhala pa ulemerero
wako, 17Pakuti ciwawa cidacitikira Lebano cidzakukuta, ndi
cionongeko ca nyama cidzakuopsa; cifukwa ca mwazi wa anthu,
ndi ciwawa cocitidwira dziko, mudzi, ndi onseokhalamo.
18Apindulanji nalo fano losema, kuti wakulipanga analisema; fano
loyenga ndi mphunzitsi wamabodza, kuti wakulipanga

alikhulupirira, ata panga matafano osanena mau? 19Tsoka iye
wakunena kwa mtengo, Galamuka; ndi kwa mwala wosalankhula,
Nyamuka Kodi ici ciphunzitsa? Taona cakutidwa ndi golidi ndi siliva,
ndi m'kati mwace mulibe mpweya konse. 20Koma Yehova ali
m'Kacisi wace wopatulika; dziko lonse lapansi ale, cete pamaso
pace.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Pemphero la Habakuku

1Pemphero la Habakuku mneneri, pa Sigionoto.
2Yehova, ndinamva mbiri yanu ndi mantha;
Yehova, tsitsimutsani nchito yanu pakati pa zaka,
Pakati pa zaka mudziwitse;
Pa mkwiyo mukumbukile cifundo.
3Mulungu anafuma ku Temani,
Ndi Woyerayo ku phiri la Parana.
Ulemerero wace unaphimba miyamba,
Ndi dziko lapansi linadzala ndi kumlemekeza.
4Ndi kunyezimira kwace kunanga kuunika;
Anali nayo mitsitsi ya dzuwa yoturuka m'dzanja lace.
Ndi komweko kunabisika mphamvu yace.
5Patsogolo pace panapita mliri,
Ndi makara amoto anaturuka pa mapaziace.
6Anaimirira, nandengulitsa dziko lapansi;
Anapenya, nanjenjemeretsa amitundu;
Ndi mapiri acikhalire anamwazika,
Zitunda za kale lomwe zinawerama;
Mayendedwe ace ndiwo a kale lomwe.
7Ndinaona mahema a Kusani ali mkusauka;
Nsaru zocinga za dziko la Midyani zinanjenjemera.
8Kodi Yehova anaipidwa nayo mitsinje?
Mkwiyo wanu unali pamitsinje kodi,
Kapena ukali wanu panyanja,
Kuti munayenda pa akavalo anu,
Pa magareta anu a cipulumutso?
9Munapombosola uta wanu;
Malumbiro analumbirira mafuko anali mau oona.
Munang'amba dziko lapansi ndi mitsinje.
10Mapiri anakuonani, namva zawawa;
Cigumula ca madzi cinapita;
Madzi akuya anamveketsa mau ace,
Nakweza manja ace m'mwamba.
11Dzuwa ndi mwezi zinaima njera mokhala mwao;
Pa kuunika kwa mibvi yanu popita iyo.
Pa kung'anipa kwa nthungo yanu yonyezimira.
12Munaponda dziko ndi kulunda,
Munapuntha amitundu ndi mkwiyo.
13Munaturukira cipulumutso ca anthu anu,
Cipulumutso ca odzozedwa anu;
Munakantha mutu wa nyumba yawoipa,
Ndi kufukula maziko kufikira m'khosi.

14Munapyoza ndi maluti ace mutu wa ankhondo ace;
Anadza ngati kabvumvulu kundimwaza;
Kukondwerera kwao kunanga kufuna kutha ozunzika mabisika.
15Munaponda panyanja ndi akavaloanu,
Madzi amphamvu anaunjikana mulu.
16Ndinamva, ndi m'mimba mwanga munabwadamuka,
Milomo yanga inanthunthumira pamau,
M'mafupa mwanga mudalowa cibvundi, ndipo ndinanjenjemera m'malo mwanga;
Kuti ndipumule tsiku lamsauko,
Pamene akwerera anthu kuti ayambane nao ndi makamu.
17Cinkana mkuyu suphuka,
Kungakhale kulibe zipatso kumpesa;
Yalephera nchito ya azitona,
Ndi m'minda m'mosapatsa cakudya;
Ndi zoweta zacotsedwa kukhola,
Palibenso ng'ombe m'makola mwao;
18Koma ndidzakondwera mwa Yehova,
Ndidzasekerera mwa Mulungu wa cipulumutso canga.
19Yehova, Ambuye, ndiye mphamvuyanga,
Asanduliza mapazi anga ngati a mbawala,
Nadzandipondetsa pa misanje yanga.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Zephaniah

Zefaniya 1

Mau oopsa akucenjeza Yerusalemu ndi Yuda

1MAU a Yehova amene anadza kwa Zefaniya mwana wa Kusi,
mwana wa Gedaliya, mwana wa Amariya, mwana wa Hezekiya,
masiku a Yosiya, mwana wa Amoni mfumu ya Yuda.
2Kuzitha ndidzazitha zonse kuzicotsa panthaka, ati
Yehova. 3Ndidzatha munthu ndi nyama; ndidzatha mbalame za
m'mlengalenga, ndi nsomba za m'nyanja, ndi zokhumudwitsa
pamodzi ndi oipa; ndipo ndidzaononga anthu kuwacotsa panthaka,
ati Yehova. 4Ndipo ndidzatambasulira dzanja langa pa Yuda, ndi pa
onse okhala m'Yerusalemu; ndipo a ndidzaononga otsala a Baala
kuwacotsa m'malo muno, ndi dzina la Akemari pamodzi ndi
ansembe; 5ndi iwo akulambira khamu la kumwamba pamwamba
pa matsindwi; ndi iwo akulambira, akulumbira pali Yehova,
nalumbiranso pali mfumu; 6ndi iwo akubwerera osamtsata Yehova;
ndi osamfuna Yehova, kapena kufunsira kwa Iye.
7Khala cete pamaso pa Ambuye Yehova; pakuti tsiku la Yehova
liyandikira; pakuti Yehova wakonzeratu nsembe, anapatula
oitanidwa ace. 8Ndipo kudzacitika tsiku la nsembe ya Yehova, kuti
ndidzalanga akalonga ndi ana a mfumu, ndi onse akubvala cobvala
cacilendo. 9Ndipo tsiku ilo ndidzalanga olumpha ciundo, nadzaza
nyumba ya mbuye wao ndi ciwawa ndi cinyengo. 10Ndipo tsiku ilo,
ati Yehova, kudzakhala phokoso lakulira locokera ku cipata
cansomba, ndi kucema kocokera ku dera laciwiri, ndi kugamuka
kwakukuru kocokera kuzitunda. 11Cemani okhala m'cigwa, pakuti
amalonda onse atayika, onsewo osenza siliva aonongeka. 12Ndipo
kudzacitika nthawi yomweyi kuti ndidzasanthula Yerusalemu ndi
nyali, ndipo ndidzalanga amunawo okhala ndi nsenga, onena
m'mtima mwao, Yehova sacita cokoma, kapena kucita
coipa. 13Ndipo zolemera zao zidzakhala zakufunkhidwa; ndi
nyumba zao zabwinja; adzamangadi nyumba, koma sadzagonamo;
adzanka minda yampesa koma sadzamwa vinyo wace. 14Tsiku
lalikuru la Yehova liri pafupi, liri pafupi lifulumira kudza, mau a
tsiku la Yehova; munthu wamphamvu adzalirapo mowawa
mtima. 15Tsikulo ndi tsiku la mkwiyo, tsiku la msauko ndi lopsinja
tsiku la bwinja, ndi cipasuko, tsiku la mdima ndi la cisisira, tsiku la
mitambo ndi lakuda bii; 16tsiku la lipenga ndi lakupfuulira midzi
yamalinga, ndi nsanja zazitali za kungondya. 17Ndipo
ndidzatengera anthu zowapsinja, kuti adzayenda ngati anthu
a'khungu, popeza anacimwira Yehova; ndi mwazi wao
udzatsanulidwa ngati pfumbi, ndi nyama yao idzanga
ndowe. 18Ngakhale siliva wao, ngakhale golidi wao sizidzakhoza

kuwalanditsa tsiku la mkwiyo wa Yehova; koma dziko lonse lidzatha ndi moto wa nsanje yace; pakuti adzacita cakutsiriza, mofulumira, onse okhala m'dziko.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Mau akucenjeza amitundu ena

1Dzisanthuleni, inde santhulani; inu mtundu wosakhumba
kanthu; 2lamulo lisanabale, tsiku lisanapitirire ngati mungu,
usanakugwereni mkwiyo waukali wa Yehova, lisanakugwereni tsiku
la mkwiyo wa Yehova. 3Funani Yehova, ofatsa inu nonse a m'dziko,
amene munacita ciweruzo cace; funani cilungamo, funani cifatso;
kapena mudzabisika tsiku la mkwiyo wa Yehova. 4Pakuti Gaza
adzasiyidwa, ndi Asikeloni adzakhala bwinja; adzaingitsa Asidodi
usana, ndi Ekroni adzazulidwa. 5Tsoka, okhala m'dziko la kunyanja,
mtundu wa Akereti! Mau a Yehova atsutsana nawe, Kanani, dziko la
Afilisti; ndidzakuononga, kuti pasakhale wokhala m'dziko. 6Ndipo
dziko la kunyanja lidzakhala husa, ndi mapanga a abusa, ndi
makola a zoweta. 7Ndipo dziko la kunyanja lidzakhala la otsala a
nyumba ya Yuda; adzadyetsa zoweta zao pamenepo; madzulo
adzagona m'nyumba za Asikeloni; pakuti Yehova Mulungu wao
adzawazonda, nadzabweza undende wao. 8Ndinamva kutonza kwa
Moabu ndi matukwano a ana a Amoni, zimene anatonza nazo
anthu anga, ndi kudzikuza pa malire ao. 9Cifukwa cace, pali moyo
wanga, ati Yehova wa makamu, Mulungu wa Israyeli, Zedi Moabu
adzakhala ngati Sodomu, ndi ana a Amoni ngati Gomora, pocuruka
khwisa ndi maenje a mcere, ndi bwinja losatha; otsala a anthu
anga adzalanda zao, ndi otsala amtundu wa anthu anga
adzawalandira akhale colowa cao. 10Ici adzakhala naco m'malo
mwa kudzikuza kwao, cifukwa anatonza, nadzikuza pa anthu a
Yehova wa makamu. 11Yehova adzawakhalira woopsa; pakuti
adzaondetsa milungu yonse ya pa dziko lapansi; ndipo
adzamlambira Iye, yense pamalo pace, a m'zisumbu zonse za
amitundu. 12Inunso Akusi, mudzaphedwa ndi lupanga
langa. 13Ndipo adzatambasulira dzanja lace kumpoto nadzaononga
Asuri, nadzasanduliza Nineve akhale bwinja, wouma ngati
cipululu. 14Ndipo zoweta zidzagona pansi pakati pace; nyama
zonse za mitundu mitundu; ndi bvuo ndi nungu zidzakhala m'mitu
ya nsanamira zace; adzayimba mau ao m'mazenera; paziundo
padzakhala cipasuko; pakuti anagadamula nchito yace ya
mkungudza. 15Uwu ndi mudzi wosekererawo unakhala
wosasamalira, unanena m'mtima mwace, Ine ndine, ndi wopanda
ine palibe wina; ha! wasanduka bwinja, mogonera nyama za
kuthengo! yense wakuupitirira adzatsonya mtsonyo, ndi kupukusa
mutu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Mau akudzudzula Yerusalemu. Malonjezo a kwa okhulupirika otsala

1Tsoka uyo wopanduka, ndi wodetsedwa, ndiye mudzi
wozunza! 2Sanamvera mau, sanalola kulangizidwa; sanakhulupirira
Yehova, sanayandikira kwa Mulungu wace. 3Akalonga ace m'kati
mwace ndiwo mikango yobangula; oweruza ace ndi mimbulu ya
madzulo, sasiya kanthu ka mawa. 4Aneneri ace ndiwo anthu a
matukutuku ndi onyenga; ansembe ao anaipsa malo opatulika,
napotoza cilamulo. 5Yehova pakati pace ali wolungama; sadzacita
cosalungama, m'mawa ndi m'mawa aonetsera ciweruzo cace
poyera, cosasowa kanthu; koma wosalungama sadziwa
manyazi. 6Ndaononga amitundu; nsanja zao za kungondya nza
bwinja, ndapasula miseu yao, palibe wopitapo; midzi yao
yaonongeka, palibe munthu, palibe wokhalamo. 7Ndinati, Zedi
udzandiopa Ine, udzalola kulangizidwa, kuti pokhala pace
pasaonongeke, monga mwa zonse ndamuikira; koma analawirira
mamawa, nabvunditsa macitidwe ao onse. 8Cifukwa cace,
mundilindire, ati Yehova, kufikira tsiku loukira Ine zofunkha; pakuti
ndatsimikiza mtima Ine kusonkhanitsa amitundu, kuti ndimemeze
maufumu kuwatsanulira kulunda kwanga, ndilo mkwiyo wanga
wonse waukali; pakuti dziko lonse lapansi lidzathedwa ndi moto wa
nsanje yanga. 9Pakuti pamenepo ndidzapatsa mitundu ya anthu
mlomo woyera, kuti onsewa aitanire pa dzina la Yehova
kumtumikira ndi mtima umodzi. 10Kucokera tsidya lija la mitsinje
ya Kusi ondipembedza, ndiwo mwana wamkazi wa obalalika anga,
adzabwera naco copereka canga. 11Tsiku ilo sudzacita manyazi ndi
zocita zako zonse unandilakwira nazo; pakuti pamenepo
ndidzacotsa pakati pako amene akondwera ndi kudzikuza kwako,
ndipo sudzacita kudzikuzanso m'phiri langa lopatulika. 12Koma
ndidzasiya pakati pako anthu ozunzika ndi osauka, ndipo iwo
adzakhulupirira dzina la Yehova. 13Otsala a Israyeli sadzacita
cosalungama, kapena kunena mabodza; ndi m'kamwa mwao
simudzapezeka lilime lonyenga; pakuti adzadya nadzagona pansi,
ndi palibe wakuwaopsa. 14Yimba, mwana wamkazi wa Ziyoni;
pfuula, Israyeli; kondwera nusekerere ndi mtima wonse, mwana
wamkazi wa Yerusalemu. 15Yehova wacotsa maweruzo ako,
anataya kunja mdani wako; mfumu ya Israyeli, Yehova, ali pakati
pako, sudzaopanso coipa. 16Tsiku lomwelo adzati kwa Yerusalemu,
Usaopa Ziyoni, manja anu asakhale olefuka. 17Yehova Mulungu
wako ali pakati pako, wamphamvu wakupulumutsa; adzakondwera
nawe ndi cimwemwe, adzakhala wopanda thamo m'cikondi cace;
adzasekerera nawe ndi kuyimbirapo. 18Ndidzasonkhanitsa iwo
akulirira msonkhano woikika, ndiwo a mwa iwe, amene katundu

wace anawakhalira mtonzo. 19Taonani, nthawi yomweyo ndidzacita
nao onse akuzunza iwe; ndipo ndidzapulumutsa wotsimphinayo,
ndi kusonkhanitsa wopitikitsidwayo; ndipo ndidzawaika akhale
cilemekezo ndi dzina, iwo amene manyazi ao anali m'dziko
lonse. 20Nthawi yomweyo ndidzakulowetsani, ndi nthawi yomweyo
ndidzakusonkhanitsani; pakuti ndidzakuikani mukhale dzina, ndi
cilemekezo mwa mitundu yonse ya anthu a pa dziko lapansi,
pamene ndibweza undende wanu pamaso panu, ati Yehova.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Haggai

Hagai 1

Mau akudzudzula ndi kudandaulira Ayuda amangenso Kacisi

1CAKA caciwiri ca mfumu Dariyo, mwezi wacisanu ndi cimodzi,
mau a Yehova anadza mwa Hagai mneneri kwa Zerubabele mwana
wa Sealitiyeli, ciwanga ca Yuda, ndi kwa Yoswa mwana wa
Yehozadaki, mkulu wa ansembe, ndi kuti, 2Atero Yehova wa
makamu, akuti, Anthu awa anena, Nthawi siinafike, nthawi
yakumanga nyumba ya Yehova. 3Pamenepo mau a Yehova anadza
mwa Hagai mneneri, ndi kuti, 4Kodi imeneyi ndiyo nthawi yakuti
inu nokha mukhala m'nyumba zanu zocingidwa m'katimo, ndi
nyumba iyi ikhale yopasuka? 5Cifukwa cace tsono, atero Yehova wa
makamu: Mtima wanu usamalire njira zanu. 6Mwabzala zambiri,
koma mututa pang'ono; mukudya, koma osakhuta; mukumwa,
koma osakoledwa; mudzibveka, koma palibe wofundidwa; ndi iye
wolembedwa nchito yakulipidwa alandirira kulipirako m'thumba
lobooka. 7Atero Yehova wa makamu: Mtima wanu usamalire njira
zanu. 8Kwerani ku dziko la mapiri, ndi kukwera nayo mitengo,
nimumange nyumbayi; ndipo kudzandikomera, ndipo
ndidzalemekezedwa, ati Yehova. 9Munayembekezera zambiri,
koma taonani, pang'ono; ndipo, mutabwera napo kwanu,
ndinauzirapo. Cifukwa ninji? ati Yehova wa makamu. Cifukwa ca
nyumba yanga yokhala yopasuka, ndipo nuthamangira yense
kunyumba kwace. 10M'mwemo cifukwa ca inu kumwamba kukaniza
mame, ndi nthaka ikaniza zipatso zace. 11Ndipo ndinaitana cirala
cidzere dziko, ndi mapiri, ndi tirigu, ndi vinyo, ndi mafuta, ndi
zimene ibala nthaka, ndi anthu, ndi zoweta, ndi nchito zonse za
manja.
12Pamenepo Zerubabele mwana wa Sealitiyeli, ndi Yoswa mwana
wa Yehozadaki, mkuru wa ansembe, ndi otsala onse a anthu,
anamvera mau a Yehova Mulungu wao, ndi mau a Hagai mneneri,
monga Yehova Mulungu wao adamtuma; ndipo anthu anaopa
pamaso pa Yehova. 13Ndipo Hagai mthenga wa Yehova m'uthenga
wa Yehova ananena ndi anthu, ndi kuti, Ine ndiri nanu, ati
Yehova. 14Ndipo Yehova anautsa mzimu wa Zerubabele mwana wa
Sealitiyeli, ciwanga ca Yuda, ndi mzimu wa Yoswa mwana wa
Yehozadaki, mkulu wa ansembe, ndi mzimu wa otsala onse a
anthu, ndipo anadza nagwira nchito m'nyumba ya Yehova wa
makamu, Mulungu wao, 15tsiku la makumi awiri ndi anai la mwezi,
mwezi wacisanu ndi cimodzi, caka caciwiri ca mfumu Dariyo.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Ulemerero wa Kacisi waciwiri

1Mwezi wacisanu ndi ciwiri, tsiku la makumi awiri ndi cimodzi la
mweziwo, mau a Yehova anadza mwa Hagai mneneri, ndi
kuti, 2Unenetu kwa Zerubabele, mwana wa Sealitiyeli, ciwanga ca
Yuda, ndi kwa Yoswa mwana wa Yehozadaki, mkuru wa ansembe,
ndi kwa otsala a anthu, kuti, 3Adatsala ndani mwa inu amene
anaona nyumba iyi m'ulemerero wace woyamba? ndipo muiona
yotani tsopano? Kodi siikhala m'maso mwanu ngati cabe? 4Koma
limbika tsopano, Zerubabele, ati Yehova; ulimbikenso Yoswa
mwana wa Yehozadaki, mkuru wa ansembe; ndipo mulimbike inu
nonse anthu a m'dziko, ati Yehova, ndi kucita; pakui. Ine ndiri
pamodzi ndi inu, ati Yehova wa makamu; 5monga momwe
ndinapangana nanu muja munaturuka m'Aigupto, ndi Mzimu
wanga unakhala pakati pa inu; musamaopa inu. 6Pakuti atero
Yehova wa makamu: Kamodzinso, katsala kanthawi,
ndidzagwedeza miyamba ndi dziko lapansi, ndi nyanja, ndi mtunda
womwe; 7ndipo ndidzagwedeza amitundu onse, ndi zofunika za
amitundu onse zidzafika, ndipo ndidzadzaza nyumba iyi ndi
ulemerero, ati Yehova wa makamu. 8Siliva ndi wanga, golidi ndi
wanga, ati Yehova wa makamu. 9Ulemerero wotsiriza wa nyumba
iyi udzaposa woyambawo, ati Yehova wa makamu; ndipo m'malo
muno ndidzapatsa mtendere, ati Yehova wa makamu.

Madzudzulo ndi malonjezo

10Tsiku la makumi awiri ndi anai la mwezi wacisanu ndi cinai, caka
caciwiri ca Dariyo, mau a Yehova anadza mwa Hagai mneneri, ndi
kuti, 11Atero Yehova wa makamu: Funsatu ansembe za cilamulo,
ndi kuti, 12Munthu akanyamulira nyama yopatulika m'ngudulira,
nakhudza mkate, kapena ndiwo, kapena vinyo, kapena mafuta,
kapena cakudya ciri conse, ndi ngudulira, kodi cisandulika
copatulika? Ndipo ansembe anayankha nati, Iai. 13Pamenepo Hagai
anati, Munthu wodetsedwa ndi mtembo akakhudza kanthu ka izi,
kodi kali kodetsedwa kanthuka? Ndipo ansembe anayankha nati,
Kadzakhala kodetsedwa. 14Ndipo Hagai anayankha, nati,
Momwemo anthu awa, ndi momwemo mtundu uwu pamaso panga,
ati Yehova; ndi momwemo nchito iri yonse ya manja ao; ndi ici
acipereka, ciri codetsedwa. 15Ndipo tsono, samalirani, kuyambira
lero ndi m'tsogolomo, kuti, kusanaikidwe mwala pa mwala m'Kacisi
wa Yehova, 16pamenepo ponse munthu akadza ku mulu woyenera
miyeso makumi awiri, pali khumi yokha; munthu akadza ku
coponderamo mphesa kudzatunga mbiya makumi asanu, pali
makumi awiri okha. 17Ndinakukanthani ndi cinsikwi ndi cinoni ndi
matalala m'nchito zonse za manja anu, koma simunabwerera
kudza kwa Ine, ati Yehova. 18Musamalire, kuyambira lero ndi

m'tsogolo, kuyambira tsiku la makumi awiri ndi cinai la mwezi
wacisanu ndi cinai, kuyambira tsiku lija anamanga maziko a Kacisi
wa Yehova, samalirani. 19Kodi mbeu ikali m'nkhokwe? Ngakhale
mpesa, ndi mkuyu, ndi khangaza ndi mzitona sizinabala;
kuyambira lero lino ndidzakudalitsani.

Adaniadzaonongeka, adzerubabele adzakwezeka

20Ndipo mau a Yehova anadza nthawi yaciwiri kwa Hagai tsiku la
makumi awiri la mwezi, ndi kuti, 21Nena ndi Zerubabele ciwanga
ca Yuda, kuti, Ndidzagwedeza miyamba ndi dziko lapansi; 22ndipo
ndidzagubuduza mipando yacifumu ya maufumu, ndidzaononga
mphamvu ya maufumu a amitundu; ndidzagubuduza magareta ndi
iwo akuyendapo; ndi akavalo ndi apakavalo adzatsika, yense ndi
lupanga la mbale wace. 23Tsiku lomwelo, ati Yehova wa makamu,
ndidzakutenga, Zerubabele mtumiki wanga, mwana wa Sealitiyeli,
ati Yehova, ndi kuika iwe ngati mphete yosindikizira; pakuti
ndakusankha, ati Yehova wa makamu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Zechariah

Zekariya 1

Mneneri adandaulira anthu Ayuda aleke zoipa zao

1MWEZI wacisanu ndi citatu, caka caciwiri ca Dariyo, mau a Yehova
anadza kwa Zekariya mwana wa Berekiya, mwana wa Ido mneneri,
ndi kuti, 2Yehova anakwiya kwambiri ndi makolo anu. 3Cifukwa
cace uziti nao, Atero Yehova wa makamu: Bwererani kudza kwa
Ine, ati Yehova wa makamu, ndipo Ine ndidzabwerera kudza kwa
inu, ati Yehova wa makamu. 4Musamakhala ngati makolo anu,
amenie aneneri akale anawapfuulira, nd kuti, Atero Yehova wa
makamu Bwereranitu kuleka njira zanu zoipa, ndi macitidwe anu
oipa; ko ma sanamva, kapena klimvera Ine ati Yehova. 5Makolo
anu, ali kut iwowo? ndi alieneri, akhala nd moyo kosatha
kodi? 6Koma mau anga ndi malemba anga, amene ndinalamulira
atumiki anga aneneriwo, kodi sanawapeza makolo anu? ndipo
anabwera, nati, Monga wno Yehova wa makamu analingirira
kuticitira ife, monga mwa njira zathu ndi monga mwa macitidwe
athu, momwemo anaticitira. Masomphenya oyamba:
akavalo, 7Tsiku la makumi awiri ndi cinai la mwezi wakhumi ndi
cimodzi, ndiwo mwezi wa Segati, caka caciwiri ca Dariyo, mau a
Yehova anadza kwa Zekariya mwana wa Berekiya, mwana wa Ido
mneneri, ndi kuti, 8Ndinaona usiku, taonani, munthu woyenda pa
kavalo wofiira, alikuima pakati pa mitengo yamcisu inali kunsi; ndi
pambuyo pace panali akavalo ofiira, odera ndi oyera. 9Pamenepo
ndinati, Awa ndi ciani, mbuyanga? Ndi mthenga wakulankhula ndi
ine anati kwa ine, Ndidzakuonetsa awa ndi ciani. 10Ndipo wakuima
pakati pa mitengo yamcisu anayankha, nati, Awa ndiwo amene
Yehova anawatumiza ayendeyende m'dziko. 11Ndipo iwo
anamyankha mthenga wa Yehova wakuima pakati pa mitengo
yamcisu, nati, Tayendayenda m'dziko, ndipo taonani, dziko lonse
likhala cete, lipumula. 12Ndipo mthenga wa Yehova anayankha
nati, Yehova wa makamu, mudzakhala mpaka liti osacitira cifundo
Yerusalemu, ndi midzi ya Yuda, imene munakwiya nayo zaka izi
makumi asanu ndi awiri? 13Ndipo Yehova anamyankha mthenga
wakulankhula ndi ine mau okoma, mau akutonthoza
mtima. 14Ndipo mthenga wakulankhula ndi ine anati kwa ine,
Pfuula, ndi kuti, Atero Yehova wa makamu: Ndicitira nsanje
Yerusalemu ndi Ziyoni ndi nsanje yaikuru. 15Ndipo ndikwiya nao
amitundu okhala osatekeseka ndi mkwiyo waukuru; pakuti
ndinakwiya pang'ono, ndipo anathandizira coipa, 16Cifukwa cace
atero Yehova: Ndabwera kudza ku Yerusalemu ndi zacifundo;
nyumba yanga idzamangidwamo, ndipo adzayesa Yerusalemu ndi
cingwe. 17Pfuulanso, ndi kuti, Atero Yehova wa makamu: Midzi

yanga idzalemerera ndi kufalikiranso; ndipo Yehova
adzasangalatsanso Ziyoni, nadzasankhamo Yerusalemu.
Masomphenya aciwiri: nyanga zinai ndi osula anai
18Ndipo ndinakweza maso anga, ndinapenya, taonani, nyanga
zinai. 19Ndipo ndinati kwa mthenga wakulankhula ndi ine, Izi
nziani? Ndipo anandiyankha, Izi ndi nyangazi zinabalalitsa Yuda,
Israyeli, ndi Yerusalemu. 20Ndipo Yehova anandionetsa osula
anai. 21Pamenepo ndinati, Adzeranji awa? Ndipo ananena, nati, Izi
ndi nyanga zimene zinabalalitsa Yuda, wopandanso wina
woweramutsa mutu wace; koma awa anadza kuziopsa, kugwetsa
nyanga za amitundu, amene anakwezera dziko la Yuda nyanga zao
kulimwaza.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masomphenya acitatu: Yerusalemu ayesedwa ndi cingwe

1Ndinakwezanso maso anga, ndinapenya, ndipo taonani, munthu
ndi cingwe coyesera m'dzanja lace. 2Ndipo ndinati, Upita kuti?
Ndipo anati kwa ine, Kukayesa Yerusalemu, kuona ngati citando
cace ncotani, ndi m'litali mwace motani. 3Ndipo taonani, mthenga
wolankhula nane anaturuka, ndi mthenga wina anaturuka
kukomana naye, 4nanena naye, Thamanga, lankhula ndi
mnyamata uyu, ndi kuti, M'Yerusalemu mudzakhala anthu ngati
m'midzi yopanda malinga, cifukwa ca kucuruka anthu ndi zoweta
momwemo. 5Pakuti Ine, ati Yehova, ndidzakhala kwa iye linga
lamoto pozungulira pace, ndipo ndidzakhala ulemerero m'kati
mwace. 6Haya, haya, thawani ku dziko la kumpoto, ati Yehova;
pakuti ndinakubalalitsani ngati mphepo zinai za kuthambo, ati
Yehova. 7Haya Ziyoni, thawa iwe wakukhala ndi mwana wamkazi
wa Babulo. 8Pakuti atero Yehova wa makamu: Utatha ulemererowo
ananditumiza kwa amitundu amene anakufunkhani; pakuti iye
wokhudza inu, akhudza mwana wa m'diso lace. 9Pakuti, taonani,
ndidzawayambasira dzanja langa, ndipo adzakhala zofunkha za
iwo amene anawatumikira; ndipo mudzadziwa kuti Yehova wa
makamu ananditumа. 10Yimba, nukondwere, mwana wamkazi wa
Ziyoni; pakuti taonani, ndirinkudza, ndipo ndidzakhala pakati pako,
ati Yehova. 11Ndipo amitundu ambiri adzaphatikidwa kwa Yehova
tsiku ilo, nadzakhala anthu anga; ndipo ndidzakhala pakati pako,
ndipo udzadziwa kuti Yehova wa makamu ananditumа kwa
iwe. 12Ndipo Yehova adzalandira colowa cace Yuda, ngati gawo
lace m'dziko lopatulikalo, nadzasankhanso Yerusalemu. 13Khalani
cete, anthu onse, pamaso pa Yehova; pakuti wagalamuka
mokhalira mwace mopatulika.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masomphenya acinai: Satana atsutsana ndi Yoswa, Mulungu amuyesa wolungama

1Pamenepo anandionetsa Yoswa mkulu wa ansembe alikuima
pamaso pa mthenga wa Yehova, ndi Satana alikuima pa dzanja
lace lamanja, atsutsana naye. 2Ndipo Yehova anati kwa Satana,
Yehova akudzudzula, Satana iwe; inde Yehova amene anasankha
Yerusalemu akudzudzula; uyu sindiye muuni wofumulidwa
kumoto? 3Koma Yoswa analikubvala nsaru zonyansa, naima
pamaso pa mthenga. 4Ndipo Iye anayankha nanena ndi iwo
akuima pamaso pace, ndi kuti, Mumbvule nsaru zonyansazi. Nati
kwa iye, Taona, ndakucotsera mphulupulu zako, ndipo
ndidzakubveka: zobvala za mtengo wace. 5Ndipo ndinati, Amuike
nduwira yoyera pamutu pace. Naika nduwira yoyera pamutu pace,
nambveka ndi zobvala; ndi mthenga wa Yehova
anaimirirapo, 6Ndipo mthenga wa Yehova anamcitira Yoswa
umboni, ndi kuti, 7Atero Yehova wa makamu: Ukadzayenda m'njira
zanga, ndi kusunga udikiro wanga, pamenepo udzaweruza nyumba
yanga, ndi kusunga mabwalo anga, ndipo ndidzakupatsa malo
oyendamo mwa awa oimirirapo. 8Tamvera tsono, Yoswa mkulu wa
ansembe, iwe ndi anzako akukhala pansi pamaso pako; pakuti iwo
ndiwo cizindikilo; pakuti taonani, ndidzafikitsa mtumiki wanga,
ndiye Mphukira. 9Pakuti taona, mwalawo ndinauika pamaso pa
Yoswa; pa mwala umodzi pali maso asanu ndi awiri; taonani,
ndidzaloca malocedwe ace, ati Yehova wa makamu, ndipo
ndidzacotsa mphulupulu ya dziko lija tsiku limodzi. 10Tsiku
lomwelo, ati Yehova wa makamu, mudzaitanizana yense mnansi
wace patsinde pa mpesa ndi patsinde pa mkuyu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masomphenya acisanu: coikapo nyali cagolidi ndi nyali zace

1Ndipo mthengayo adalankhula nane, anadzanso, nandiutsa ngati
munthu woutsidwa m'tulo tace. 2Ndipo anati kwa ine, Uona ciani?
Ndipo ndinati, Ndaona, taonani, coikapo nyali ca golidi yekha
yekha, ndi mbale yace pamwamba pace, ndi nyali zace zisanu ndi
ziwiri pamenepo; nyalizo zinali ndi misiwe isanu ndi iwiri, ndiyo ya
nyalizo zinali pamwamba pace; 3ndi mitengo iwiri yaazitona
pomwepo, wina ku dzanja lamanja la mbaleyo, ndi wina ku dzanja
lace lamanzere. 4Ndipo ndinayankha ndi kunena ndi mthenga
wakulankhula ndi ine, ndi kuti, Izi nziani mbuyanga? 5Ndipo
mthenga wakulankhula ndi ine anayankha, nati kwa ine, Sudziwa
kodi kuti nziani izi? Ndipo ndinati, Iai, mbuyanga. 6Pamenepo
anayankha, nanena kwa ine, ndi kuti, Awa ndi mau a Yehova kwa
Zerubabele, Ndi khamu la nkhondo ai, ndi mphamvu ai, koma ndi
Mzimu wanga, ati Yehova wa makamu. 7Ndiwe yani, phiri lalikuru
iwe? pamaso pa Zerubabele udzasanduka cidikha; ndipo
adzaturutsa mwala wa cimbudzi, ndi kupfuula, Cisomo, cisomo
nao. 8Ndipo mau a Yehova anadza kwa ine, ndi kuti, 9Manja a
Zerubabele anaika maziko a nyumba iyi, manja ace omwe
adzaitsiriza; ndipo udzadziwa kuti Yehova wa makatnu anandituma
kwa inu. 10Pakuti wapeputsa tsiku la tinthu tating'ono ndani?
pakuti adzakondwera, asanu ndi awiri awa, nadzaona cingwe
colungamitsira ciriri m'dzanja la Zerubabele, ndiwo maso a Yehova;
ayendayenda mwa dziko lonse. 11Pamenepo ndinayankha, ndinati
kwa iye, Mitengo iyi iwiri ya azitona kulamanja ndi kulamanzere
kwa coikapo nyali nciani? 12Ndipo ndinayankha kaciwiri, ndinati
naye, Nzotani nthambi ziwiri izi za azitona zirikutsanula zokha
mafuta onga golidi mwa misiwe iwiri yagolidi? 13Ndipo
anandiyankha, nati, Sudziwa kodi kuti nziani izi? Ndipo ndinati, Iai,
mbuyanga. 14Pamenepo anati, Awa ndi ana amuna awiri a mafuta
oimirira pamaso pa Mbuye wa dziko lonse lapansi.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masomphenya acisanu ndi cimodzi: mpukutu wouluka

1Pamenepo ndinakwezanso maso anga, ndinapenya, taonani,
mpukutu wouluka. 2Ndipo anati kwa ine, Uona ciani? Ndipo
ndinayankha, Ndiona mpukutu wouluka; utali wace mikono
makumi awiri, ndi citando cace mikono khumi. 3Ndipo anati kwa
ine, Ili ndi temberero lirikuturukira pa dziko lonse; pakuti ali yense
wakuba adzapitikitsidwa kuno monga mwa ili; ndi ali yense
wakulumbira zonama adzapitikitsidwa kuno monga mwa
ili. 4Ndidzaliturutsa ili, ati Yehova wa makamu, ndipo lidzalowa
m'nyumba ya wakuba, ndi m'nyumba ya iye wolumbira monama
pa dzina langa; ndipo lidzakhala pakati pa nyumba yace, ndi kuitha
pamodzi ndi mitengo yace ndi miyala yace.

Masomphenya acisanu ndi ciwiri: mkazi ndi efa

5Pamenepo mthenga wakulankhula ndi ine anaturuka, nati kwa
ine, Kwezatu maso ako, nuone ngati nciani ici
cirikuturukaci. 6Ndipo ndinati, Nciani ici? Nati iye, Ici ndi efa
alikuturuka. Natinso, Ici ndi maonekedwe ao m'dziko lonse; 7(ndipo
taonani, cozunguniza cantobvu cotukulidwa) ndipo ici ndi mkazi
wokhala pakati pa efa. 8Ndipo anati, Uyu ndi ucimo; namgwetsa
m'kati mwa efa; naponya ntobvu wolemerawo pakamwa
pace. 9Pamenepo ndinakweza maso anga, ndinapenya, ndipo
taonani, anaturuka akazi awiri, ndi m'mapiko mwao munali
mphepo; ndipo anali nao mapiko ngati mapiko a cumba,
nanyamula efayo pakati pa dziko ndi thambo. 10Ndipo ndinati kwa
mthenga wakulankhula ndi ine, Amenewa amuka naye kuti
efayo? 11Ndipo anati kwa ine, Kummangira nyumba m'dziko la
Sinara; kuti amuike, namkhazikeko pa kuzika kwace.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masomphenya acisanu ndi citatu: magareta anai

1Ndipo ndinakwezanso maso anga, ndinapenya, ndipo taonani,
anaturuka magareta anai pakati pa mapiri awiri; ndi mapiriwo
ndiwo mapiri amkuwa. 2Ku gareta woyamba kunali akavalo ofiira;
ndi ku gareta waciwiri akavalo akuda; 3ndi ku gareta wacitatu
akavalo oyera; ndi ku gareta wacinai akavalo olimba
amawanga. 4Ndipo ndinayankha ndinati kwa mthenga wolankhula
ndi ine, Izi nziani, mbuyanga? 5Ndi mthenga anayankha, nati kwa
ine, Izi ndi mphepo zinai zakumwamba zakuturuka kumene
zimaimirira pamaso pa Ambuye wa dziko lonse lapansi. 6Gareta wa
akavalo akuda aturukira ku dziko la kumpoto; ndi oyerawo
aturukira kuwatsata; ndi amawanga aturukira ku dziko la
kumwela. 7Ndi amphamvuwo anaturuka nayesa kumka
kuyendayenda m'dziko; pakuti adati, Mukani, yendayendani
m'dziko. Momwemo anayendayenda m'dziko. 8Ndipo anandiitana,
nanena nane, kuti, Taonani, iwo akuturuka kumka ku dziko la
kumpoto anapumulitsa Mzimu wanga m'dziko lakumpoto.

Akorona a Yoswa

9Ndipo mau a Yehova anadza kwa ine, ndi kuti, 10Tenga a iwo a
kundende, a Keledai, a Tobiya, ndi a Yedaya; nudze tsiku lomwelo,
nulowe ku nyumba ya Yosiya, mwana wa Zefaniya, kumene
anafikirako kucokera ku Babulo, 11ndipo utenge siliva ndi golidi,
nupange akorona, nuwaike pamutu pa Yoswa mwana wa
Yehozadaki mkuru wa ansembe; 12nunene naye, kuti, Atero Yehova
wa makamu, ndi kuti, Taonani, munthu dzina lace ndilo Mphukira,
ndipo adzaphuka m'malo mwace, nadzamanga Kacisi wa
Yehova: 13inde adzamanga Kacisi wa Yehova; nadzasenza
ulemererowo, nadzakhala ndi kulamulira pa mpando wacifumu
wace; nadzakhala wansembe pampando wacifumu wace; ndi
uphungu wa mtendere udzakhala pakati pa iwo awiri, 14Ndipo
akorona adzakhala wa Kelemu, ndi wa Tobiya, ndi wa Yedaya, ndi
wa Keni mwana wa Zefaniya, akhale cikumbutso m'Kacisi wa
Yehova. 15Ndipo iwo akukhala kutari adzafika, nadzamanga ku
Kacisi wa Yehova, ndipo inu mudzadziwa kuti Yehova wa makamu
ananditumiza kwa inu. Ndipo ici cidzacitika ngati mudzamvera
mwacangu mau a Yehova Mulungu wanu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Kusala kosalamulidwa ndi Yehova

1Ndipo kunacitika caka cacinai ca mfumu Dariyo, mau a Yehova anadza kwa
Zekariya tsiku lacinai la mwezi wacisanu ndi cinai, ndiwo Kisilevi. 2Ndipo a ku
Beteli anatuma Sarezere ndi Regemeleke ndi anthu ao, apepeze
Yehova, 3nanene kwa ansembe a nyumba ya Yehova wa makamu, ndi kwa
aneneri, ndi kuti, Kodi ndilire mwezi wacisanu, ndi kudzipatula, monga umo
ndikacitira zaka izi zambiri? 4Ndipo mau a Yehova wa makamu anadza kwa
ine, ndi kuti, 5Nena kwa anthu onse a m'dziko, ndi kwa ansembe, kuti, Muja
mukasala ndi kulira mwezi wacisanu, ndi wacisanu ndi citatu, zaka izi makumi
asanu ndi awiri, kodi mukasalira Ine, Inedi? 6Ndipo pamene mukadya, ndi
pamene mukamwa, mukadya si ndinu, mukamwa si ndinu kodi? 7Si ndiwo
mau Yehova anawalalikira mwa aneneri oyamba aja, muja Yerusalemu anali
nao okhalamo, ndi wokhazikika; ndi m'midzi mwace pozungulira pace, ndi
m'dziko la kumwela, ndi m'cidikha munali anthu okhalamo?
8Ndipo mau a Yehova anadza kwa Zekariya, ndi kuti, 9Watero Yehova wa
makamu, kuti, Weruzani ciweruzo coona, nimucitire yense mnzace cifundo ndi
ukoma mtima; 10musazunza mkazi wamasiye, kapena ana amasiye, mlendo
kapena waumphawi; ndipo nnena mmodzi wa inu alingirire m'mtima mwace
kumcitira coipa munthu mnzace. 11Koma anakana kumvera, nakaniza phewa
lao, natseka makutu ao, kuti asamve. 12Inde, anasanduliza mitima yao ikhale
ngati mwala woti gwa, kuti angamve cilamulo, ndi mau amene Yehova wa
makamu anatumiza ndi Mzimu wace mwa aneneri oyamba aja; m'menemo
munafuma mkwiyo waukuru wocokera kwa Yehova wa makamu. 13Ndipo
kunacitika, monga Iye anapfuula, koma iwo sanamvera; momwemo iwo
adzapfuula, koma Ine sindidzamva, ati Yehova wa makamu; 14koma
ndidzawabalalitsa ndi kabvumvulu mwa amitundu onse amene sanawadziwa.
Motero dziko linakhala bwinja, m'mbuyo mwao; palibe munthu wopitapo ndi
kubwererako; pakuti adaika dziko lofunikalo labwinja.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Madalitso olonjezedwa ndi Mulungu

1Ndipo mau a Yehova wa makamui anadza kwa ine, ndi kuti, 2Atero
Yehova wa makamu: Ndimcitira nsanje Ziyoni ndi nsanje yaikuru,
ndipo ndimcitira nsanje ndi ukali waukuru. 3Atero Yehova:
Ndabwerera kudza ku Ziyoni, ndidzakhala pakati pa Yerusalemu;
ndi Yerusalemu adzachedwa, Madzi wa coonadi; ndi phiri la Yehova
wa makamu, Phiri lopatulika. 4Atero Yehova wa makamu: M'miseu
ya Yerusalemu mudzakhalanso amuna ndi akazi okalamba, yense
ndi ndodo yace m'dzanja lace cifukwa ca ukalamba wace. 5Ndi
m'miseu ya mudzi mudzakhala ana amuna ndi akazi akusewera
m'miseu yace. 6Atero Yehova wa makamu: Cikakhala codabwitsa
pamaso pa otsala a anthu awa masiku awo, kodi cidzakhalanso
codabwitsa pamaso panga? ati Yehova wa makamu. 7Atero Yehova
wa makamu: Taonani, ndidzapulumutsa anthu anga m'dziko la
kum'mawa, ndi m'dziko la kumadzulo; 8ndipo ndidzabwera nao,
nadzakhala m'kati mwa Yerusalemu; ndipo iwo adzakhala anthu
anga, nanenso ndidzakhala Mulungu wao, m'coonadi ndi
m'cilungamo. 9Atero Yehova wa makamu: Alimbike manja anu, inu
akumva masiku ano mau awa pakamwa pa aneneri amene
anakhalako tsiku lakuikidwa maziko a nyumba ya Yehova wa
makamu, ndiyo Kacisi, kuti amangidwe. 10Pakuti asanafike masiku
aja, panalibe kulipidwira munthu, kapena kulipidwira nyama, ndipo
analibe mtendere iye wakuturuka, kapena wakulowa, cifukwa ca
wosautsa; pakuti ndinatumiza munthu yense atsutsane naye
mnzace. 11Koma tsopano sindidzakhala kwa otsala a anthu awa
monga momwe ndinakhalira masiku oyamba, ati Yehova wa
makamu. 12Pakuti padzakhala mbeu ya mtendere; mpesa
udzapatsa zipatso zace, ndi nthaka idzapatsa zobala zace, ndi
miyamba Idzapatsa mame ao; ndipo ndidzalandiritsa otsala a
anthu awa izi zonse, cikhale colowa cao. 13Ndipo kudzacitika kuti,
monga munali cotembereretsa mwa amitundu, inu nyumba ya
Yuda, ndi nyumba ya Israyeli, momwemo ndidzakusungani, ndipo
mudzakhala codalitsa naco; musaope, alimbike manja
anu. 14Pakuti atero Yehova wa makamu: Monga ndil nalingirira
kucitira inu coipa, muja makolo anu anautsa mkwiyo wanga, ati
Yehova wa makamu, ndipo sindinawaleka; 15momwemonso
ndinalingirira masiku ano kucitira cokoma Yerusalemu ndi nyumba
ya Yuda; musaopa. 16Izi ndizo muzicite: Nenani coonadi yense ndi
mnzace; weruzani zoona ndi ciweruzo ca mtendere m'zipata
zanu; 17ndipo musalingirira coipa m'mtima mwanu yense pa
mnzace; nimusakonde lumbiro lonama; pakuti izi zonse ndidana
nazo, ati Yehova.

18Ndipo mau a Yehova wa makamu anadza kwa ine, ndi
kuti, 19Atero Yehova wa makamu: Kusala kwa mwezi wacinai, ndi
kusala kwa mwezi wacisanu, ndi kusala kwa mwezi wacisanu ndi
ciwiri, ndi kusala kwa mwezi wakhumi kukhale kwa nyumba ya
Yuda cimwemwe ndi cikondwerero, ndi nyengo zoikika zosekerera;
cifukwa cace kondani coonadi ndi mtendere. 20Atero Yehova wa
makamu: Kudzacitikanso kuti mitundu ya anthu, ndi okhalamo
m'midzi yambiri adzafika, 21ndi okhala m'mudzi umodzi adzamuka
ku mudzi wina, ndi kuti, Tiyeni msanga kukapepeza Yehova, ndi
kufunafuna Yehova wa makamu; ndimuka inenso. 22Inde, mitundu
yambiri ya anthu, ndi amitundu amphamvu adzadza kufunafuna
Yehova wa makamu m'Yerusalemu, ndi kupepeza Yehova. 23Atero
Yehova wa makamu: Kudzacitika masiku awo amuna khumi
adzagwira, ndiwo a manenedwe onse a amitundu, inde adzagwira
mkawo wa munthu ali Myuda, ndi kuti, Tidzamuka nanu, pakuti
tamva kuti Mulungu ali ndi inu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Kulangidwa kwa amitundu ena

1Katundu wa mau a Yehova pa dziko la Hadraki, ndipo Damasiko
adzakhala popumula pace; pakuti Yehova apenyerera anthu monga
apenyerera mafuko onse a Israyeli; 2ndi Hamati yemwe
wogundana naye malire; Turo ndi Zidoni, angakhale ali ndi nzeru
zambiri. 3Ndipo Turo adzadzimangira polimbikirapo, nadzakundika
siliva ngati pfumbi, ndi golidi woyenga ngati thope la
kubwalo. 4Taonani, Yehova adzamlanda zace, nadzakantha
mphamvu yace igwe m'manja; ndipo adzatha ndi moto. 5Asikeloni
adzaciona, nadzaopa; Gazanso, nadzanjenjemera kwambiri; ndi
Ekroni, pakuti ciyembekezo cace cacitidwa manyazi; ndipo mfumu
idzatayika ku Gaza, ndi Asikeloni adzasowa okhalamo. 6Ndi mtundu
wa anthu osokonezeka udzakhala m'Asidodi, ndipo ndidzaononga
kudzikuza kwa Afilisti. 7Ndipo ndidzacotsa mwazi wace m'kamwa
mwace, ndi zonyansa zace pakati pa mano ace; momwemo iyenso
adzakhala wotsalira wa Mulungu wathu, ndipo adzakhala ngati
mkuru wa pfuko m'Yuda, ndi Ekroni ngati Myebusi. 8Ndipo
ndidzamangira nyumba yanga misasa, kuiletsera nkhondo,
asapitepo munthu kapena kubweranso; ndipo wakuwasautsa
sadzapitanso pakati pao; pakuti tsopano ndapenya ndi maso anga.
9Kondwera kwambiri, mwana wamkazi wa Ziyoni; pfuula mwana
wamkazi wa Yerusalemu; taona, Mfumu yako ikudza kwa iwe; ndiye
wolungama, ndi mwini cipulumutso; wofatsa ndi wokwera pa buru,
ndi mwana wamphongo wa buru. 10Ndipo ndidzaononga magareta
kuwacotsa m'Efraimu, ndi akavalo kuwacotsa m'Yerusalemu; ndi
uta wa nkhondo udzaonongeka; ndipo adzanena zamtendere kwa
amitundu; ndi ufumu wace udzakhala kuyambira kunyanja kufikira
nyanja, ndi kuyambira ku Mtsinje kufikira malekezero a
dziko. 11Iwenso, cifukwa ca mwazi wa pangano lako ndinaturutsa
andende ako m'dzenje m'mene mulibe madzi. 12Bwererani kudza
kulinga, andende a ciyembekezo inu; ngakhale lero lino ndilalikira
kuti ndidzakubwezera cowirikiza. 13Pakuti ndadzikokera Yuda,
ndadzaza uta ndi Efraimu; ndipo ndidzautsa ana ako, Ziyoni,
alimbane nao ana ako, Yavani, ndipo ndidzakuyesa lupanga la
ngwazi. 14Ndipo Yehova adzaoneka pamwamba pao, ndi mubvi
wace udzaturuka ngati mphezi; ndipo Ambuye Mulungu adzaomba
lipenga, nadzayenda ndi akabvumvulu a kumwela. 15Yehova wa
makamu adzawacinjiriza; ndipo adzadza, nadzapondereza miyala
yoponyera; ndipo adzamva, nadzacita phokoso ngati avinyo; ndipo
adzadzazidwa ngati mbale, ngati ngondya za guwa la
nsembe. 16Ndipo Yehova Mulungu wao adzawapulumutsa tsiku ilo,
ngati zoweta za anthu ace; pakuti adzakhala ngati miyala ya
m'korona yakunyezimira pa dziko lace. 17Pakuti ukoma wace ndi

waukuru ndithu, ndi kukongola kwace nkwa kukuru ndithu! tirigu adzakometsera anyamata, ndi vinyo watsopano anamwali.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Malonjezo a kwa Israyeli

1Pemphani kwa Yehova mvula, m'nyengo ya mvula ya masika, kwa Yehova
wolenga mphezi; ndipo adzawapatsa mibvumbi ya mvula, kwayense
zophukira kuthengo. 2Pakuti aterafi anena zopanda pace, ndi aula aona
bodza; nafotokoza maloto acabe, asangalatsa nazo zopanda pace; cifukwa
cace ayendayenda ngati nkhosa, azunzika popeza palibe mbusa. 3Mkwiyo
wanga wayakira abusa, ndipo ndidzalanga atonde; pakuti Yehova wa makamu
adzazonda zoweta zace, ndizo nyumba ya Yuda, nadzaziika ngati kavalo wace
waulemerero kunkhondo. 4Kwa iye kudzafuma mwala wa kungondya, kwa iye
msomali, kwa iye uta wankhondo, kwa iye osautsa onse pamodzi. 5Ndipo
adzakhala ngati ngwazi zakupondereza adani m'thope la kubwalo kunkhondo;
ndipo adzacita nkhondo, cifukwa Yehova ali nao; ndi apakavalo adzacitidwa
manyazi. 6Ndipo ndidzalimbitsa nyumba ya Yuda, ndi kusunga nyumba ya
Yosefe, ndipo ndidzawakhalitsa, pakuti ndawacitira cifundo; ndipo adzakhala
monga ngati sindinawataya konse; pakuti Ine ndine Yehova Mulungu wao,
ndipo ndidzawamvera. 7Ndipo iwo a ku Efraimu adzakhala ngati ngwazi, ndi
mtima wao udzakondwera ngati ndi vinyo; ndipo ana ao adzaciona
nadzakondwera; mtima wao udzakondwerera mwa Yehova. 8Ndidzawayimbira
mluzu ndi kuwasonkhanitsa, pakuti ndawaombola; ndipo adzacuruka monga
anacurukira kale. 9Ndipo ndidzawafesa mwa mitundu ya anthu, ndipo
adzandikumbukila m'maiko akutali; nadzakhala pamodzi ndi ana ao,
nadzabwera. 10Ndidzawatenganso ku dziko la Aigupto, ndi kuwasonkhanitsa
m'Asuri; ndipo ndidzalowa nao m'dziko la Gileadi ndi Lebano; koma
sadzawafikira. 11Ndipo adzapita pakati pa nyanja ya nsautso, nadzapanda
mafunde a m'nyanja, ndi maiwe onse a mtsinje adzaphwa; ndi kudzikuza kwa
Asuri kudzagwetsedwa; ndi ndodo yacifumu ya Aigupto idzacoka. 12Ndipo
ndidzawalimbitsa mwa Yehova; ndipo adzayendayendam'dzina lace, ati
Yehova.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Kulangidwa kwa osalapa

1Tsegula pa makomo ako Lebano, kuti moto uthe mikungudza
yako. 2Cema, mtengo wamlombwa, pakuti mkungudza wagwa,
popeza mitengo yokoma yaipitsidwa; cemani athundu a ku Basani,
pakuti nkhalango yocinjirizika yagwa pansi. 3Mau a kucema kwa
abusa! pakuti ulemerero wao waipsidwa; mau a kubangula kwa
misona ya mikango! pakuti kudzikuza kwa Yordano
kwaipsidwa. 4Atero Yehova Mulungu wanga: Dyetsani zoweta
zakukaphedwa; 5zimene eni ace azipha, nadziyesera osaparamula;
ndi iwo akuwagulitsa akuti, Alemekezedwe Yehova, pakuti ine
ndine wolemera; ndi abusa ao sazicitira cifundo. 6Pakuti
sindidzacitiranso cifundo okhala m'dzikomo, ati Yehova; koma
taonani, ndidzapereka anthu, yense m'dzanja la mnansi wace, ndi
m'dzanja la mfumu yace; ndipo iwo adzakantha dzikoli, ndi
m'dzanja mwao sindidzawalanditsa. 7M'mwemo ndinadyetsa
zoweta zakukaphedwa, ndizo zoweta zonyankhalala. Ndipo
ndinadzitengera ndodo ziwiri; yina ndinaicha Cisomo, inzace
ndinaicha Comanganitsa; ndipo ndinadyetsa zowetazo. 8Ndipo
ndinatha abusa atatuwo mwezi umodzi; pakuti mtima wanga
unalema nao, ndi mtima waonso unaipidwa nane. 9Pamenepo
ndinati, Sindidzadyetsanso inu; cirikufa cife; cosoweka cisoweke;
ndi zotsala zidyane, conse nyama ya cinzace. 10Ndipo ndinatenga
ndodo yanga Cisomo, ndi kuidula pakati, kuti ndiphwanye pangano
langa ndinalicita ndi mitundu yonse ya anthu. 11Ndipo linatyoka
tsikulo, momwemo zonyankhalala za zoweta, zakundisamalira Ine,
zinadziwa kuti ndiwo mau a Yehova. 12Ndipo ndinanena nao,
Cikakomera inu, ndipatseni mphotho yanga; ngati iai, lekani. Ndipo
anayesa mphotho yanga, kulemera kwace ndarama zasiliva
makumi atatu. 13Ndipo Yehova anati kwa ine, Kaziponye kwa
woumba mbiya, mtengo wace wokometsetsa anandiyesawo. Ndipo
ndinatenga ndarama makumi atatu asiliva, ndi kuziponya kwa
woumba mbiya, m'nyumba ya Yehova. 14Pamenepo ndinadula
ndodo yanga yina, ndiyo Comanganitsa, kuti ndithetse cibale ca
pakati pa Yuda ndi Israyeli.
15Ndipo Yehova anati kwa ine, Dzitengerenso zipangizo za mbusa
wopusa. 16Pakuti taonani, ndidzautsa mbusa m'dziko amene
sadzazonda otayika, kapena kufunafuna zomwazika, kapena
kulunzitsa yotyoka, kapena kudyetsa yamoyo, koma adzadya
nyama ya zonenepa, nadzang'amba ziboda zao. 17Tsoka mbusa
wopanda pace, wakusiya zoweta! lupanga pa dzanja lace, ndi pa
diso lace la kumanja; dzanja lace lidzauma konse, ndi diso lace
lamanja lidzada bii.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Ukulu wa Israyeli m'tsogolo

1Katundu wa mau a Yehova wakunena Israyeli.
Atero Yehova, wakuyala miyamba, ndi kuika maziko a dziko
lapansi, ndi kulenga mzimu wa munthu m'kati mwace; 2Taonani,
ndidzaika Yerusalemu akhale cipanda codzandiritsa kwa mitundu
yonse ya anthu yozungulirapo, ndipo cidzafikira Yuda yemwe
pomangira misasa Yerusalemu. 3Ndipo kudzacitika tsiku ilo,
ndidzaika Yerusalemu akhale mwala wolemetsa mitundu yonse ya
anthu; onse akuusenza adzadzilasa nao; ndi amitundu onse a pa
dziko lapansi adzasonkhana kutsutsana nao. 4Tsiku ilo, ati Yehova,
ndidzakantha kavalo ali yense ndi kumdabwitsa, ndi womkwera
adzayaluka; ndipo ndidzatsegulira maso anga nyumba ya Yuda, ndi
kukantha kavalo ali yense wa mitundu ya anthu akhale
wakhungu. 5Ndipo akalonga a Yuda adzanena m'mtima mwao,
Okhala m'Yerusalemu ndiwo mphamvu yanga m'Yehova wa
makamu Mulungu wao. 6Tsiku ilo ndidzaika akalonga a Yuda ngati
phale la moto pansi pa nkhuni, ndi ngati muuni wamoto mwa
mitolo ya tirigu; ndipo adzatha mitundu yonse ya anthu
pozungulirapo, ku dzanja lamanja ndi lamanzere; ndipo Yerusalemu
adzakhalanso m'malo mwace, m'Yerusalemu. 7Ndipo Yehova
adzayamba kupulumutsa mahema a Yuda, kuti ulemerero wa
nyumba ya Davide ndi ulemerero wa okhala m'Yerusalemu
usakulire Yuda. 8Tsiku ilo Yehova adzacinjiriza okhala
m'Yerusalemu; ndi iye wokhumudwa pakati pao tsiku lomwelo
adzakhala ngati Davide; ndi nyumba ya Davide idzakhala ngati
Mulungu, ngati mthenga wa Yehova pakati pao. 9Ndipo kudzacitika
tsiku lomwelo, ndidzayesa kuononga amitundu onse akudza
kuyambana ndi Yerusalemu. 10Ndipo ndidzatsanulira pa nyumba ya
Davide, ndi pa okhala m'Yerusalemu, mzimu wa cisomo ndi
wakupembedza; ndipo adzandipenyera Ine amene anandipyoza;
nadzamlira ngati munthu alira mwana wace mmodzi yekha,
nadzammvera zowawa mtima, monga munthu amvera zowawa
mtima mwana wace woyamba. 11Tsiku lomwelo kudzakhala maliro
akuru m'Yerusalemu, ngati maliro a Hadadirimoni m'cigwa ca
Megidoni, 12Ndipo dziko lidzalira, banja liri lonse pa lokha; banja la
nyumba ya Davide pa lokha, ndi akazi ao pa okha; banja la
nyumba ya Natani pa lokha, ndi akazi ao pa okha; 13banja la
nyumba ya Levi pa lokha, ndi akazi ao pa lokha; banja la Asimei pa
okha, ndi akazi ao pa okha; 14mabanja onse otsala, banja liri lonse
pa lokha, ndi akazi ao pa okha.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Kuyeretsedwa kwa Yerusalemu

1Tsiku lomwelo padzatsegukira nyumba ya Davide ndi okhala
m'Yerusalemu kasupe wa kwa ucimo ndi cidetso. 2Ndipo
kudzacitika tsiku lomwelo, ati Yehova wa makamu, ndidzaononga
maina a mafano m'dziko; ndipo sadzakumbukikanso; ndipo
ndidzacotsa m'dziko aneneri ndi mzimu wacidetso. 3Ndipo
kudzacitika, akaneneranso wina, atate wace ndi mai wace ombala
adzanena naye, Sudzakhala ndi moyo, pakuti unena bodza m'dzina
la Yehova; ndipo atate wace ndi mai wace ombala adzamgwaza
ponenera iye. 4Ndipo kudzacitika tsiku lomwelo kuti aneneri
adzacita manyazi yense ndi masomphenya ace, ponenera iye;
ndipo sadzabvala copfunda caubweya kunyenga naco; 5koma
adzati, Sindiri mneneri, ndiri wolima munda; pakuti munthu
anandiyesa kapolo kuyambira ubwana wanga. 6Ndipo wina akati
kwa iye, Zipsera izi m'manja mwako nza ciani? adzayankha, Ndizo
za mabala anandilasa m'nyumba ya ondikonda.
7Galamuka, lupanga, pa mbusa wanga, ndi pa munthu mnzanga
wa pamtima, ati Yehova wa makamu; kantha mbusa, ndi nkhosa
zidzabalalika; koma ndidzabwezera dzanja langa pa
zazing'onozo. 8Ndipo kudzacitika m'dziko lonse, ati Yehova,
magawo awiri m'menemo adzalikhidwa nadzafa; koma gawo
lacitatu lidzasiyidwa m'mwemo. 9Ndi gawo lacitatulo
ndidzalitengera kumoto, ndi kuwayenga ngati ayenga siliva, ndi
kuwayesa monga ayesa golidi; adzaitana dzina langa, ndipo
ndidzawamvera; ndidzati, Awa ndi anthu anga; ndi iwo adzati,
Yehova ndi Mulungu wanga.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Yehova adzathandiza a ku Yerusalemu polimbana ndi amitundu

1Taonani likudza tsiku la Yehova, limene zofunkha zako
zidzagawanika pakati pako. 2Pakuti ndidzasonkhanitsa amitundu
onse alimbane ndi Yerusalemu; ndipo mudziwo udzalandidwa, ndi
nyumba zidzafunkhidwa, ndi akazi adzakakamizidwa; ndi limodzi la
magawo awiri la mudzi lidzaturuka kumka kundende, koma anthu
otsala sadzaonongeka m'mudzimo. 3Pamenepo Yehova adzaturuka,
nadzacita nkhondo ndi amitundu aja, monga anacitira nkhondo
tsiku lakudumana. 4Ndi mapazi ace adzaponda tsiku lomwelo pa
phiri la Azitona, liri pandunji pa Yerusalemu kum'mawa, ndi phiri la
Azitona lidzang'ambika pakati kuloza kum'mawa ndi kumadzulo,
ndipo padzakhala cigwa cacikuru; ndi gawo lina la phirilo
lidzamuka kumpoto, ndi gawo lina kumwela. 5Pamenepo
mudzathawa kudzera cigwa ca mapiri anga; pakuti cigwa ca mapiri
cidzafikira ku Azali; ndipo mudzathawa monga umo munathawira
cibvomezi, masiku a Uziya mfumu ya Yuda; ndipo Yehova Mulungu
wanga adzadza, ndi opatulika onse pamodzi ndi Inu. 6Ndipo
kudzacitika tsiku lomwelo, sikudzakhala kuunika, zowalazo
zidzada; 7koma lidzakhala tsiku la pa lokha lodziwika ndi Yehova;
palibe usana, palibe usiku; koma kudzatero kuti madzulo kudzati
mbe. 8Ndipo kudzacitika tsiku lomwelo kuti madzi amoyo
adzaturuka ku Yerusalemu; gawo lao lina kumka ku nyanja ya
kum'mawa, ndi gawo lina kumka ku nyanja ya kumadzulo;
adzatero nyengo ya dzinja ndi ya mwamvu.

Yehova mfumu ya dziko lonse lapansi

9Ndipo Yehova adzakhala mfumu ya dziko lonse; tsiku lomwelo
Yehova adzakhala Iye yekha, ndi dzina lace ilo lokha. 10Dziko lonse
lidzasandulika, lidzanga cidikha, kuyambira ku Geba kufikira ku
Rimoni, kumwela kwa Yerusalemu; ndipo pali uwupo padzakhala
ponyamuka, ndipo udzakhala m'malo mwace, kuyambira ku cipata
ca Benjamini kufikira ku malo a cipata coyamba, kufikira ku cipata
ca kungondya, ndi kuyambira nsanja ya Hananeli kufikira ku
zoponderamo mphesa za mfumu. 11Ndipo anthu adzakhala
m'menemo, ndipo sipadzakhalanso kuonongetsa; koma
Yerusalemu adzakhala mosatekeseka. 12Ndipo mliri umene Yehova
adzakantha nao mitundu yonse ya anthu imene idathira nkhondo
pa Yerusalemu ndi uwu: nyama yao idzaonda akali ciriri pa mapazi
ao, ndi maso ao adzapuala m'pfunkha mwao, ndi lilime lao
lidzanyala m'kamwa mwao. 13Ndipo kudzali tsiku lomwelo, kuti
cisokonezo cacikuru cocokera kwa Yehova cidzakhala pakati pao;
ndipo adzagwira yense dzanja la mnzace; ndi dzanja lace
lidzaukira dzanja la mnzace. 14Ndi Yuda yemwe adzacita nkhondo

ku Yerusalemu; ndi zolemera za amitundu onse ozungulirapo zidzasonkhanizidwa, golidi, ndi siliva, ndi zobvala zambirimbiri. 15Momwemonso mliri wa pa akavalo, nyuru, ngamila, ndi aburu, ndi nyama zonse zokhala m'misasa iyo, udzakhala ngati mliri uwo. 16Ndipo kudzacitika kuti otsala onse a amitundu onse anadzawo kulimbana ndi Yerusalemu, adzakwera caka ndi caka kulambira mfumu Yehova wa makamu, ndi kusunga madyerero amisasa. 17Ndipo kudzacitika kuti ali yense wa mabanja a dziko wosakwera kumka ku Yerusalemu kulambira mfumu Yehova wa makamu, pa iwowa sipadzakhala mvula. 18Ndipo banja la ku Aigupto likapanda kukwera, losafika, sirdzawagwera kodi mliri umene Yehova adzakantha nao amitundu osakwera kusunga madyerero amisasa? 19Ili ndi cimo la Aigupto, ndi cimo la amitundu onse osakwerako kusunga madyerero a misasa. 20Tsiku lomwelo padzaoneka pa miriu ya akavalo OPATULIKIRA YEHOVA; ndi mbiya za m'nyumba ya Yehova zidzanga mbale za ku guwa la nsembe. 21Inde mbiya zonse za m'Yerusalemu ndi m'Yuda zidzakhala zopatulikira Yehova wa makamu; ndi onse akuphera nsembe adzafika nadzatengako, ndi kuphikamo; ndipo tsiku lomwelo simudzakhalanso Mkanani m'nyumba ya Yehova wa makamu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Zoipa za Israyeli; aneneratu kuti adzalangidwa

1Tamverani mau awa akunenerani Yehova motsutsa, inu ana a
Israyeli, kulinenera banja lonse ndinalikweza kuliturutsa m'dziko la
Aigupto, ndi kuti, 2Inu nokha ndinakudziwani mwa mabanja onse a
pa dziko lapansi, m'mwemo ndidzakulangani cifukwa ca
mphulupulu zanu zonse. 3Kodi awiri adzayenda pamodzi
asanapanganiranetu? 4Kodi mkango udzabangula m'nkhalango
wosakhala nayo nyama? Kodi msona wa mkango udzalira m'ngaka
mwace usanagwire kanthu? 5Kodi mbalame idzakodwa
mumsampha pansi popanda msampha woichera? Kodi msampha
ufamphuka pansi wosakola kanthu? 6Kodi adzaomba lipenga
m'mudzi osanieniemera anthu? Kodi coipa cidzagwera mudzi
osacicita Yehova? 7Pakuti Ambuye Yehova sadzacita kanthu
osaulula cinsinsi cace kwa atumiki ace aneneri. 8Mkango
ukabangula, ndani amene saopa? Ambuye Yehova wanena, ndani
amene sanenera?
9Bukitsani ku nyumba zacifumu za Asidodi, ndi ku nyumba
zacifumu za m'dziko la Aigupto, nimuziti, Sonkhanani pa mapiri a
Samariya, ndipo penyani masokosero akuru m'menemo, ndi
ozunzika m'kati mwace. 10Pakuti sadziwa kucita zolungama, amene
akundika zaciwawa ndi umbala m'nyumba zao zacifumu, ati
Yehova. 11Cifukwa cace, atero Ambuye Yehova, Padzakhala mdani
pozungulira pace pa dziko, nadzatsitsa kukucotsera mphamvu
yako; ndi za m'nyumba zako zacifumu adzazifunkha. 12Atero
Yehova, Monga mbusa alanditsa m'kamwa mwa mkango miyendo
iwiri, kapena kansonga ka khutu, momwemo adzalanditsidwa ana
a Israyeli okhala pansi m'Samariya, m'ngondya ya guwa logonapo,
ndi pa mitsamiro ya kama. 13Tamverani inu, mucitire umboni
wotsutsa nyumba ya Yakobo, ati Ambuye Yehova Mulungu wa
makamu. 14Pakuti tsiku lakumlanga Israyeli cifukwa ca zolakwa
zace, ndidzalanganso maguwa a nsembe a ku Beteli; ndi nyanga
za guwa la nsembe zidzadulidwa, nizidzagwa pansi. 15Ndipo
ndidzakantha nyumba ya nyengo yacisanu, pamodzi ndi nyumba
ya nyengo yadzuwa; ndi nyumba zaminyanga zidzaonongeka; ndi
nyumba zazikuruzo zidzatha, ati Yehova.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Aisrayeli adzadulidwa cifukwa ca zoipa ndi kuuma mtima kwao

1Tamverani mau awa, inu ng'ombe zazikazi za ku Basana, zokhala
m'phiri la Samariya, zosautsa aumphawi, zopsinja osowa, zonena
kwa ambuyao, Bwerani naco, timwe. 2Ambuye Yehova walumbira
pali ciyero cace, kuti taonani, adzakugwerani masiku akuti
adzakucotsani ndi zokowera, ndi otsala anu ndi mbedza. 3Ndipo
mudzaturukira popasuka linga, yense m'tsogolo mwace, ndi
kutayika ku Harimoni, ati Yehova.
4Idzani ku Beteli, mudzalakwe ku Giligala, nimucurukitse zolakwa,
nimubwere nazo nsembe zanu zophera m'mawa ndi m'mawa,
magawo anu akhumi atapita masiku atatu atatu; 5nimutenthe
nsembe zolemekeza zacotupitsa, nimulalikire nsembe zaufulu, ndi
kuzimveketsa; pakuti ici mucikonda, inu ana a Israyeli, ati Ambuye
Yehova. 6Ndipo ine ndakupatsaninso mano oyera m'midzi yanu
yonse, ndi kusowa mkate m'malo mwanu monse; koma
simunabwerera kudza kwa Ine, ati Yehova. 7Ndipo Ine
ndakumanani mvula, itatsala miyezi itatu isanafika nyengo
yakukolola; ndipo ndinabvumbistira mudzi umodzi mvula,
osabvumbitsira mudzi wina; munda wina unabvumbidwa mvula,
ndi m'munda mosabvumbidwa mvula munafota. 8M'mwemo midzi
iwiri kapena itatu inayenda peyupeyu ku mudzi umodzi kukamwa
madzi, koma sanakhuta; koma simunai bwerera kudza kwa Ine, ati
Yehova. 9Ndinakukanthani ndi cinsikwi ndi cinoni; minda yanu
yocuruka yamipesa, ndi yamikuyu, ndi yaazitona, yaonongeka ndi
cirimamine; koma simunabwerera kudza kwa Ine, ati
Yehova. 10Ndinatumiza mliri pakati panu monga m'Aigupto;
anyamata anu ndawapha ndi lupanga, ndi kutenga akavalo anu;
ndipo ndinakweretsa kununkha kwa cigono canu kufikitsa
kumphuno kwanu; ikoma simunabwerera kudzakwa Ine, ati
Yehova. 11Ndinagubuduza ena mwa inu, monga umo Mulungu
anagubuduzira Sodomu ndi Gomora; ndipo inu munali ngati muuni
wofumulidwa kumoto; koma simunabwerera kudza kwa Ine, ati
Yehova. 12Cifukwa cace ndidzatero nawe, Israyeli; popeza
ndidzakucitira ici, dzikonzeretu kukomana ndi Mulungu wako,
Israyeli. 13Pakuti taona, Iye amene aumba mapiri, nalenga
mphepo, nafotokozera munthu maganizo ace, nasanduliza
m'mawa ukhale mdima, naponda pa misanje ya dziko lapansi,
dzina lace ndiye Yehova Mulungu wamakamu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Nyimbo ya maliro yakunena za kutyoka kwa Israyeli

1Tamverani mau awa ndinenawa, akhalire inu nyimbo ya maliro,
nyumba ya Israyeli inu. 2Namwali wa Israyeli wagwa, sadzaukanso;
wagwetsedwa pa nthaka yace, palibe womuutsa. 3Pakuti atero
Ambuye Yehova, M'nyumba ya Israyeli, mudzi woturukamo cikwi
cimodzi adzautsalira zana limodzi, ndi uwu woturukamo zana
limodzi adzautsalira khumi. 4Pakuti atero Yehova kwa nyumba ya
Israyeli, Mundifunefune Ine, ndipo mudzakhala ndi moyo; 5koma
musamafuna Beteli, kapena kumalowa m'Giligala; musamapita ku
Beereseba; pakuti Giligala adzalowadi m'ndende, ndi Beteli
adzasanduka cabe. 6Funani Yehova, ndipo mudzakhala ndi mayo;
angabuke ngati moto m'nyumba ya Yosefe, ndipo unganyeke
wopanda wakuzima m'Beteli; 7inu osintha ciweruzo cikhale
civumulo, nimugwetsa pansi cilungamo, 8Iye wakulenga Nsangwe
ndi Akamwiniatsatana, nasanduliza mdima wandiweyani ukhale
m'mawa, nasanduliza usana ude ngati usiku, wakuitana madzi a
m'nyanja, nawatsanulira pa dziko lapansi, dzina lace ndiye
Yehova; 9wakufikitsa cionongeko pa wamphamvu modzidzimuka,
cionongeko nicigwera linga, 10Iwo adana naye wodzudzula
kucipata, nanyansidwa naye wolunjikitsa mau. 11Popeza tsono
mupondereza aumphawi, ndi kumsonkhetsa tirigu; mwamanga
nyumba za miyala yosema, koma simudzakhala m'mwemo;
mwaoka minda ya mipesa yokonda, koma simudzamwa vinyo
wace. 12Pakuti ndidziwa kuti zolakwa zanu nzocuruka, ndi macimo
anu ndi olimba, inu akusautsa olungama, akulandira cokometsera
mlandu, akukankha osowa kucipata. 13Cifukwa cace wocenierayo
akhala cete nthawi yomweyo; pakuti ndiyo nthawi yoipa. 14Funani
cokoma, si coipa ai; kuti mukhale ndi moyo; motero Yehova
Mulungu wamakamu adzakhala ndi inu, monga munena. 15Danani
naco coipa, nimukonde cokoma; nimukhazikitse ciweruzo kucipata;
kapena Yehova Mulungu wa makamu adzacitira cifundo otsala a
Yosefe. 16Cifukwa cace atero Yehova, Mulungu wa makamu,
Ambuye, M'makwalala onse mudzakhala kulira, ndi m'miseu yonse
adzati, Kalanga ine! kalanga ine! nadzaitana wakumunda adze
kumaliro, ndi odziwa maliridwe a nthetemya alire. 17Ndi m'minda
yonse yamipesa mudzakhala kulira, pakuti ndipita pakati pako, ati
Yehova. 18Tsoka inu akufuna tsiku la Yehova! mudzapindulanji nalo
tsiku la Yehova? ndilo mdima, si kuunika ai. 19Kudzakhala monga
munthu akathawa mkango, ndi cimbalangondo cikomana naye;
kapena akalowa m'nyumba, natsamira kukhoma ndi dzanja lace,
nimluma njoka. 20Kodi tsiku la Yehova silidzakhala la mdima, si la
kuunika ai? lakuda bii, lopanda kuwala m'menemo? 21Ndidana nao,
ndinyoza madyerero anu, sindidzakondwera nao masonkhano anu

oletsa. 22Inde, mungakhale mupereka kwa Ine nsembe zanu
zopsereza, ndi nsembe zaufa, sindidzazilandira Ine; ndinsembe
zoyamika za ng'ombe zanu zonenepa, sindidzazisamalira
Ine. 23Mundicotsere phokoso la nyimbo zanu; sindifuna kumva
mayimbidwe a zisakasa zanu. 24Koma ciweruzo ciyende ngati
madzi, ndi cilungamo ngati mtsinje wosefuka. 25Ngati munabwera
nazo kwa Ine nsembe zophera ndi zaufa zaka makumi anai
m'cipululu, inu nyumba ya Israyeli? 26Inde mwasenza hema wa
mfumu yanu, ndi tsinde la mafano anu, nyenyezi ya mlungu wanu,
amene mudadzipangira. 27M'mwemo ndidzakutengani kumka nanu
kundende kutsogolo kwa Damasiko, ati Yehova, amene dzina lace
ndiye Mulungu wa makamu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Aisrayeli otsata zilakolako zao adzapsinjika ndi mtundu wina wa anthu

1Tsoka osalabadirawo m'Ziyoni, ndi iwo okhazikika m'phiri la
Samariya, ndiwo anthu omveka amtundu woposa wa anthu, amene
nyumba ya Israyeli iwafikira! 2Pitani ku Kaline, nimuone; kucokera
komweko mupite ku Hamati wamkulu mutsikire ku Gati wa Afilisti;
kodi awo ndi okoma koposa maufumu ano? kapena malire ao
aposa malire anu? 3Inu akutalikitsa tsiku loipa, ndi kusendeza
pafupi mpando waciwawa; 4ogona pa makama aminyanga,
nadzithinula pa maguwa ao ogonapo, nadya ana a nkhosa a ku
zoweta, ndi ana a ng'ombe ocoka pakati pa khola; 5akungoyimba
kutsata maliridwe a zeze, nadzilingiririra zoyimbira nazo Ingati
Davide; 6akumwera vinyo m'zipanda, nadzidzoza ndi mafuta
abwino oposa, osagwidwa cisoni ndi kutyoka kwa Yosefe. 7Cifukwa
cace tsono, adzatengedwa ndende ndi oyamba kutengedwa
ndende; ndi phokoso la iwo odzithinula lidzapita. 8Ambuye Yehova
walumbira pali Iye mwini, ati Yehova Mulungu wa makamu,
Ndinyansidwa nako kudzikuza kwa Yakobo, ndidana nazo nyumba
zace zacifumu; m'mwemo ndidzapereka mudzi, ndi zonse ziri
m'menemo. 9Ndipo kudzacitika, mukatsala amuna khumi
m'nyumba imodzi, adzafa. 10Ndipo mbalewace wa munthu
akamnyamula, ndiye womtentha, kuturutsa mafupa m'nyumba,
nakati kwa iye ali m'kati mwa nyumbamo, Atsala wina nawe kodi?
nakati, lai; pamenepo adzati, Khala cete; pakuti sitingachule dzina
la Yehova. 11Pakuti taonani, Yehova walamulira, nadzakantha
nyumba yaikuru icite mpata, ndi nyumba yaing'ono icite
mindala. 12Kodi akavalo adzathamanga pathanthwe? kodi
adzalimako ndi ng'ombe? pakuti mwasanduliza ciweruzo cikhale
ndulu, ndi cipatso ca cilungamo cikhale civumulo; 13inu okondwera
naco copanda pace, ndi kuti, Kodi sitinadzilimbitsa tokha mwa
mphamvu yathu yathu? 14Pakuti taonani, ndidzakuutsirani mtundu
wa anthu, nyumba ya Israyeli, ati Yehova Mulungu wa makamu;
ndipo adzakupsinjani kuyambira polowera ku Hamati kufikira
mtsinje wa kucidikha.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masomphenya atatu, dzombe, moto wonyambita, ndi cingwe: colungamitsa ciriri

1Ambuye Yehova anandionetsa cotere; ndipo taonani, anaumba
dzombe, poyamba kuphuka kwa maudzu a cibwereza; ndipo
taonani, ndico cibwereza atawasengera mfumu. 2Ndipo kunacitika
m'mene lidatha kudya msipu wa dziko, ndinati, Ambuye Yehova,
khululukiranitu Yakobo; adzakhala ciriri bwanji? popeza ndiye
wamng'ono. 3Ndipo Yehova anacileka. Sicidzacitika, ati Yehova.
4Ambuye Yehova anandionetsa cotere; ndipo taonani, Ambuye
Yehova anaitana kuti atsutse ndi moto; ndipo unanyambita
cakudya cacikuru ukadanyambitanso dziko. 5Pamenepo ndinati,
Ambuye Yehova, Iekanitu; Yakobo adzakhala ciriri bwanji? pakuti ali
wamng'ono. 6Ndipo Yehova anacileka. Ici comwe sicidiacitika, ati
Ambuye Yehova.
7Anandionetsa cotere; ndipo taonani, Ambuye anaima pa khoma
lomangiwda ndi cingwe colungamitsira ciriri; ndi cingwe
colungamitsira ciriri m'dzanja lace. 8Ndipo Yehova anati kwa ine,
Amosi, uona ciani? Ndipo ndinati, Cingwe colungamitsira ciriri. Nati
Ambuye, Taona, ndidzaika cingwe colungamitsira ciriri pakati pa
anthu anga Israyeli, sindidzawalekanso: 9ndi misanje ya Isake
idzakhala bwinja; ndi malo opatulika a Israyeli adzapasuka; ndipo
ndidzaukira nyumba ya Yerobiamu ndi lupanga.

Amosi ndi Amaziya atsutsana ku Beteli

10Pamenepo Amaziya wansembe wa ku Beteli anatumiza kwa
Yerobiamu mfumu ya Israyeli, ndi kuti, Amosi wapangira inu
ciwembu pakati pa nyumba ya Israyeli; dziko silikhoza kulola mau
ace onse. 11Pakuti atero Amosi, Yerobiamu adzafa ndi lupanga, ndi
Israyeli adzatengedwadi ndende, kucoka m'dziko lace. 12Amaziya
anatinso kwa Amosi, Mlauli iwe, coka, thawira ku dziko la Yuda,
nudye, nunenere komweko; 13koma usaneneranso ku Beteli; pakuti
pamenepo mpa malo opatulika a mfumu, ndiyo nyumba
yacifumu. 14Pamenepo Amosi anayankha, nati kwa Amaziya,
Sindinali mneneri, kapena mwana wa mneneri, koma ndinali
woweta ng'ombe, ndi wakuchera nkhuyu; 15ndipo Yehova
ananditenga ndirikutsata nkhosa, nati kwa ine Yehova, Muka,
nenera kwa anthu anga Israyeli. 16Cifukwa cace tsono, tamvera
mau a Yehova, Iwe ukuti, Usamanenera cotsutsana ndi Israyeli,
usadonthetsa mau akutsutsana ndi nyumba ya Isake; 17cifukwa
cace atero Yehova, Mkazi wako adzakhala wadama m'mudzi, ndi
ana ako amuna ndi akazi adzagwa ndi lupanga, ndi dziko lako
lidzagawanidwa ndi kuyesa cingwe, ndi iwe mwini udzafa m'dziko
lodetsedwa; ndipo Israyeli adzatengedwadi ndende kucoka m'dziko
lace.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masomphenya a mtanga wa zipatso, Zoopsa za pa Israyeli

1Ambuye Yehova anandionetsa cotere; ndipo taonani, mtanga wa
zipatso zamalimwe. 2Ndipo anati, Amosi uona ciani? Ndipo ndinati,
Mtanga wa zipatso zamalimwe. Nati Yehova kwa ine, Citsiriziro
cafikira anthu anga Israyeli, sindidzawalekanso. 3Koma nyimbo za
kukacisi zidzasanduka kubuma tsiku ilo, ati Ambuye Yehova;
mitembo idzacuruka; adzaitaya pali ponse padzakhala
zii. 4Tamverani ici, inu akumeza aumphawi, ndi kuwatha ofatsa
m'dziko, ndi kuti, 5Mwezi wokhala upita liti, kuti tigulitse dzinthu?
ndi Sabata, kuti titsegulire tirigu? ndi kucepsa efa, ndi kukuliitsa
sekeli, ndi kucenjerera nayo miyeso yonyenga; 6kuti tigule osauka
ndi ndarama, ndi aumphawi ndi nsapato, ndi kugulitsa nsadwa za
tirigu. 7Yehova walumbira pali kudzikuza kwa Yakobo, Ngati
ndidzaiwala konse nchito zao ziri zonse? 8Kodi dziko
silidzanjenjemera cifukwa ca ici, ndi kulira ali yense wokhalamo?
inde lidzakwera lonseli ngati madzi a m'mtsinje; lidzagwedezeka,
ndi kutsikanso ngati mtsinje wa Aigupto, 9Ndipo kudzacitika tsiku
lomwelo, ati Ambuye Yehova, ndidzalowetsa dzuwa usana, ndi
kudetsa dziko pausana poyera. 10Ndipo ndidzasanduliza madyerero
anu, akhale maliro, ndi nyimbo zanu zikhale za maliro, ndi kufikitsa
ziguduli m'cuuno monse, ndi mpala pa mutu uli wonse; nadzakhala
ngati maliro a mwana mmodzi yekha, ndi citsiriziro cace ngati tsiku
lowawa. 11Taonani, akudza masiku, ati Ambuye Yehova, akuti
ndidzatumiza njala m'dzikomo, si njala ya mkate kapena ludzu la
madzi, koma njala ya kumva mau a Yehova. 12Ndipo
adzayendayenda peyupeyu kuyambira kunyanja kufikira kunyanja
ndi kuyambira kumpoto kufikira kum'mawa;
adzathamangathamanga kufunafuna mau a Yehova, koma
osawapeza. 13Tsiku lomwelo anamwali okongola ndi anyamata
adzakomoka nalo ludzu. 14Iwo akulumbira ndi kuchula cimo la
Samariya, ndi kuti, Pali Mulungu wako, Dani; ndipo, Pali moyo wa
njira ya ku Beereseba, iwowa adzagwa, osaukanso konse.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Masomphenya a kulangidwa koopsa. Lonjezo kuti madalitso adzabwera

1Ndinaona Ambuye alikuima pa guwa la nsembe, nati Iye, Kantha
mitu ya nsanamira, kuti ziundo zigwedezeke; nuphwanye mitu yao
yonse; ndipo ndidzapha otsiriza ao ndi lupanga; wothawayo mwa
iwo sadzathawadi, ndi wopulumukayo
mwaiwosadzapulumukadi. 2Angakhale akumba mpaka kunsi kwa
manda, dzanja langa lidzawatenga kumeneko; angakhale akwera
kumwamba, ndidzawatsitsa komweko. 3Angakhale abisala
pamwamba pa Karimeli, ndidzawapwaira ndi kuwatenga komweko;
angakhale abisala pamaso panga pansi pa nyanja, kumeneko
ndidzalamulira njoka, ndipo idzawaluma. 4Angakhale alowa ndende
pamaso pa adani ao, kumeneko ndidzalamulira lupanga, ndipo
lidzawapha; ndipo ndidzayang'anitsa maso anga kwa iwowa,
kuwacitira coipa, si cokoma ai. 5Pakuti Ambuye Yehova wa
makamu ndiye amene akhudza dziko, nilisungunuka; ndi onse
okhalamo adzacita maliro; ndipo lidzakwera lonseli ngati madzi a
m'nyanja; nilidzatsikanso ngati nyanja ya m'Aigupto; 6ndiye amene
amanga zipinda zace zosanja m'mwamba, nakhazika tsindwi lace
pa dziko lapansi; Iye amene aitana madzi a m'nyanja,
nawatsanulira padziko; dzina lace ndiye Yehova. 7Kodi simukhala
kwa Ine ngati ana a Kusi, inu ana a Israyeli? ati Yehova.
Sindinakweza Israyeli ndine, kumturutsa m'dziko la Aigupto, ndi
Afilisti ku Kafitori, ndi Aaramu ku Kiri? 8Taonani, maso a Ambuye
Yehova ali pa ufumu wocimwawo, ndipo ndidzauononga kuucotsa
pa dziko lapansi; pokhapo sindidzaononga nyumba ya Yakobo
kuitha konse, ati Yehova. 9Pakuti taonani, ndidzalamulira, ndipo
ndidzapeta nyumba ya Israyeli mwa amitundu onse, monga apeta
tirigu m'licero; koma silidzagwa pansi diso, ndi limodzi
lonse. 10Ocimwa onse a anthu anga adzafa ndi lupanga, ndiwo
amene akuti, Coipa sicidzatipeza, kapena kutidulira.
11Tsiku lomwelo ndidzautsa msasa wa Davide udagwawo, ndi
kukonzanso zopasuka zace; ndipo ndidzautsa zogumuka zace, ndi
kuumanga monga masiku a kalelo; 12kuti alandire otsala a Edomu
akhale colowa cao, ndi amitundu onse akuchedwa dzina langa, ati
Yehova wakucita izi. 13Taonani akudza masiku, ati Yehova, akud
wolima adzapezana ndi wodula, ndi woponda mphesa adzapezana
ndi wofesa, ndi mapiri adzakhetsa vinyo watsopano, ndi zitunda
zonse zidzasungunuka. 14Ndipo ndidzabwezanso undende wa
anthu anga Israyeli, ndipo adzamanganso mabwinja, ndi kukhala
m'menemo; nadzaoka minda ya mipesa nadzamwa vinyo wace,
nadzalima minda ndi kudya zipatso zace. 15Ndipo ndidzawaoka

m'dziko mwao ndipo sadzazulidwanso m'dziko lao limene ndawapatsa, ati Yehova Mulungu wako.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Malachi

Malaki 1

Kusayamika kwa Israyeli pa cikondi ca Mulungu

1KATUNDU wa mau a Yehova wa kwa Israyeli mwa Malaki.
2Ndakukondani, ati Yehova; koma inu mukuti, Mwatikonda motani? Esau si mkulu wace wa Yakobo kodi? ati Yehova; ndipo ndinakonda Yakobo; 3koma Esau ndinamuda, ndinasanduliza mapiri ace abwinja, ndi kupereka colowa cace kwa ankhandwe a m'cipululu. 4Cinkana Edomu akuti, Taphwanyika, koma tidzabwera ndi kumanganso mabwinja; atero Yehova wa makamu, Adzamanga, koma Ine ndidzapasula; ndipo adzawacha, Dziko la coipa, ndiponso, Anthu amene Yehova akwiya nao cikwiyire. 5Ndipo maso anu adzaona, nimudzati, Yehova ali wamkuru kupitirira malire a Israyeli.
6Mwana alemekeza atate wace, ndi mnyamata mbuye wace; ngati Ine tsono ndine atate, uli kuti ulemu wanga? ngati Ine ndine mbuye, kundiopa kuli kuti? ati Yehova wa makamu kwa inu ansembe akupeputsa dzina langa. Ndipo mukuti, Tapeputsa dzina lanu motani? 7Mupereka mkate wodetsedwa pa guwa langa la nsembe; ndipo mukuti, Takudetsani motani? M'menemo, mwakuti munena, Gome la Yehova nlonyozeka. 8Ndipo pamene mupereka yakhungu ikhale nsembe, mukuti, Palibe coipa! ndi popereka yotsimphina ndi yodwala, palibe coipa! Kaiperekeni kwa kazembe wanu, mudzamkomera kodi? kapena adzakubvomerezani kodi? ati Yehova wa makamu. 9Ndipo tsopano, mupepeze Mulungu, kuti aticitire cifundo; icico cicokera kwa inu; kodi Iye adzabvomereza ena a inu? ati Yehova wa makamu. 10Mwenzi atakhala wina mwa inu wakutseka pamakomo, kuti musasonkhe moto cabe pa guwa langa la nsembe! Sindikondwera nanu, ati Yehova wa makamu, ndipo sindidzalandira capereka m'dzanja lanu. 11Pakuti kuyambira koturukira dzuwa kufikira kolowera kwace dzina langa lidzakhala lalikuru mwa amitundu; ndipo m'malo monse adzaperekera dzina langa cofukiza ndi copereka coona; pakuti dzina langa lidzakhala lalikuru mwa amitundu, ati Yehova wa makamu. 12Koma inu muliipsa, pakunena inu, Gome la Yehova laipsidwa, ndi zipatso zace, cakudya cace, conyozeka. 13Mukutinso, Taonani, ncolemetsa ici! ndipo mwacipeputsa, ati Yehova wa makamu; ndipo mwabwera nazo zofunkha, ndi zotsimphina, ndi zodwala; momwemo mubwera nayo nsembe; kodi ndiyenera kuilandira ku dzanja lanu? ati Yehova. 14Koma wotembereredwa wonyengayo, wokhala nayo yaimuna m'gulu lace, nawinda, naphera Yehova nsembe cinthu cacirema; pakuti Ine ndine mfumu yaikuru, ati Yehova wa makamu; ndipo dzina langa ndi loopsa pakati pa amitundu.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Mau akutsutsa ansembe

1Ndipo tsono, ansembe inu, lamulo ili ndi la kwa inu. 2Mukapanda
kumvera, mukapanda kuliika mumtima mwanu, kupatsa dzina
langa ulemerero, ati Yehova wa makamu, ndidzakutumizirani
temberero, ndi kutemberera madalitso anu; inde, ndawatemberera
kale cifukwa simuliika mumtima. 3Taonani, ndidzaipsa mbeu
cifukwa ca inu, ndi kuwaza ciphwidza pankhope panu, ndico
ciphwidza ca nsembe zanu, ndipo adzakucotsani pamodzi
naco. 4Ndipo mudzadziwa kuti ndatumiza lamulo ili kwa inu, kuti
cipangano canga cikhale ndi Levi, ati Yehova wa
makamu. 5Cipangano canga cinali naye ca moyo ndi ca mtendere;
ndipo ndinampatsa izi kuti aope; nandiopa, naopsedwa cifukwa ca
dzina langa. 6Cilamulo ca zoona cinali m'kamwa mwace, ndi
cosalungama sicinapezeka m'milomo mwace; anayenda nane
mumtendere ndi moongoka, nabweza ambiri aleke
mphulupulu, 7Pakuti milomo ya wansembe iyenera kusunga
cidziwitso, ndi anthu ayenera kufunafuna cilamulo pakamwa pace;
pakuti iye ndiye mthenga wa Yehova wa makamu. 8Koma inu
mwapambuka m'njira; mwakhumudwitsa ambiri m'cilamulo;
mwaipsa cipangano ca Levi, ati Yehova wa makamu. 9Cifukwa cace
Inenso ndakuikani onyozeka ndi ocepseka kwa anthu onse, popeza
simunasunga njira zanga, koma munaweruza mwankhope pocita
cilamulo.

Za kukwatira akazi acilendo, Za kuleka mkazi kosayenera

10Kodi sitiri naye Atate mmodzi ife tonse? sanatilenga kodi
Mulungu mmodzi? Ticita monyengezana yense ndi mnzace cifukwa
ninji, ndi kuipsa cipangano ca makolo athu? 11Yuda wacha
monyenga, ndi m'Israyeli ndi m'Yerusalemu mwacitika conyansa;
pakuti Yuda waipsa cipatuliko ca Yehova cimene acikonda,
nakwatira mwana wamkazi wa mlungu wacilendo. 12Yehova
adzalikha munthu wakucita ici, wogalamutsa ndi wobvomereza
m'tnahema a Yakobo, ndi iye wopereka copereka kwa Yehova wa
makamu. 13Ndi ici mubwereza kucicita: mukuta guwa la nsembe la
Yehova ndi misozi, ndi kulira, ndi kuusa moyo; momwemo Iye
sasamaliranso copereka, kapena kulandira mokondwera m'dzanja
lanu. 14Koma mukuti, Cifukwa ninji? Cifukwa kuti Yehova anali
mboni pakati pa iwe ndi mkazi wa ubwana wako, amene
unamcitira cosakhulupirika, cinkana iye ndiye mnzako, mkazi wa
pangano lako. 15Ndipo sanatero kodi wina womtsalira mzimu?
Ndipo winayo anatero bwanji? Anatero pofuna mbeu ya Mulungu.
Koma sungani mzimu wanu; ndipo asamcitire monyenga mkazi wa
ubwana wace ndi mmodziyense. 16Pakuti ndidana nako kuleka

kumene, ati Yehova Mulungu wa Israyeli, ndi iye wakukuta cobvala cace ndi ciwawa, ati Yehova wa makamu; cifukwa cace sungani mzimu wanu kuti musacite mosakhulupirika.
17Mwalemetsa Yehova ndi mau anu. Koma mukuti, Tamlemetsa ndi ciani? Ndi ici cakuti munena, Yense wakucita coipa ali wokoma pamaso pa Mulungu, ndipo akondwera nao; kapena, Ali kuti Mulungu wa ciweruzo?

©The Bible Society of Malawi, 1992

Za mthenga wokonzeratu njira ya Ambuye

1Taonani, nditumа mthenga wanga, kuti akonzeretu njira pamaso
panga; ndipo Ambuye amene mumfuna adzadza ku Kacisi wace
modzidzimutsa; ndiye mthenga wa cipangano amene mukondwera
naye; taonani akudza, ati Yehova wa makamu. 2Koma ndani
adzapirira tsiku la kudza kwace? ndipo adzaima ndani pooneka
Iye? pakuti adzanga moto wa woyenga, ndi sopo wa otsuka; 3ndipo
adzakhala pansi ndi kuyenga ndi kuyeretsa siliva, nadzayeretsa
ana a Levi, nadzawayengetsa ngati golidi ndi siliva; pamenepo iwo
adzapereka kwa Yehova zopereka m'cilungamo. 4Pamenepo
copereka ca Yuda ndi Yerusalemu cidzakomera Yehova, ngati
masiku a kale lija ndi ngati zaka zoyamba zija. 5Ndipo
ndidzayandikiza kwa inu kuti ndiweruze; ndipo ndidzakhala mboni
yakufulumira kutsutsa obwebweta, ndi acigololo, ndi olumbira
monama; ndi iwo akunyenga wolembedwa nchito pa kulipira
kwace, akazi amasiye, ndi ana amasiye, ndi wakuipsa mlandu wa
mlendo, osandiopa Ine, ati Yehova wa makamu. 6Pakuti Ine Yehova
sindisinthika, cifukwa cace inu ana a Yakobo simunathedwa.

Za kusalanda za Mulungu ndi madalitso atsatapo

7Kuyambira masiku a makolo anu mwapambuka kuleka malemba
anga osawasunga. Bwererani kudza kwa Ine, ndipo Ine
ndidzabwerera kwa inu, ati Yehova wa makamu. Koma inu mukuti,
Tibwerere motani? 8Kodi munthu adzalanda za Mulungu? ndipo inu
mundilanda Ine. Koma mukuti, Takulandani zotani? Limodzi limodzi
la magawo khumi, ndi zopereka. 9Mutembereredwa ndi temberero;
pakuti mundilanda Ine, ndinu mtundu uwu wonse. 10Mubwere nalo
limodzi limodzi lonse la khumi, ku nyumba yosungiramo, kuti
m'nyumba mwanga mukhale cakudya; ndipo mundiyese nako
tsono, ati Yehova wa makamu, ngati sindikutsegulirani mazenera a
kumwamba, ndi kukutsanulirani mdalitso wakuti adzasoweka malo
akuulandira. 11Ndipo ndidzadzudzula zolusa cifukwa ca inu, kuti
zisakuononger eni zipatso za nthaka yanu; ngakhale mpesa wanu
sudzayoyoka zipatso zace, zosaca m'munda, ati Yehova wa
makamu. 12Ndipo amitundu onse adzacha inu odala; pakuti
mudzakhala dziko lokondweretsa, ati Yehova wa makamu.
13Mau anu andilimbira, ati Yehova. Koma inu mukuti, Tanena
motsutsana nanu ndi ciani? 14Mwanena, Kutumikira Mulungu nkwa
cabe; ndipo tapindulanji ndi kusunga udikiro wace, ndi kuyenda
obvala zamaliro pamaso pa Yehova wa makamu? 15Ndipo tsopano
tiwacha odzikuza odala, inde iwo ocita zoipa amangidwa ngati
nyumba; inde, ayesa Mulungu, napulumuka. 16Pamenepo iwo
akuopa Yehova analankhulana wina ndi mnzace; ndipo Yehova
anawachera khutu namva, ndi buku la cikumbutso linalembedwa

pamaso pace, la kwa iwo akuopa Yehova, nakumbukila dzina
lace. 17Ndipo adzakhala anga anga, ati Yehova wa makamu, tsiku
ndidzaikalo, ndipo ndidzawaleka monga munthu aleka mwana
wace womtumikira. 18Pamenepo mudzabwera ndi kuzindikira
pakati pa wolungama ndi woipa, pakati pa iye wotumikira Mulungu
ndi iye wosamtumikira.

©The Bible Society of Malawi, 1992

Oipa adzalangidwa, okoma adzadalitsidwa. Asamale cilamulo; adzafika Eliya

1Pakuti taonani, likudza tsiku, lotentha ngati ng'anjo; ndipo onse
akudzikuza ndi onse akucita coipa, adzakhala ngati ciputu; ndi
tsiku lirinkudza lidzawayatsa, ati Yehova wa makamu, osawasiyira
muzu kapena nthambi. 2Koma inu akuopa dzina langa, dzuwa la
cilungamo lidzakuturukirani, muli kuciritsa m'mapiko mwace; ndipo
mudzaturuka ndi kutumphatumpha ngati ana a ng'ombe
onenepa, 3Ndipo mudzapondereza oipa; pakuti adzakhala ngati
mapulusa ku mapazi anu, tsiku ndidzaikalo, ati Yehova wamakamu.
4Kumbukilani cilamulo ca Mose mtumiki wanga, ndinamlamuliraco
m'Horebu cikhale ca Israyeli lonse, ndico malemba ndi
maweruzo. 5Taonani, ndidzakutumizirani Eliya mneneri lisanadze
tsiku lalikuru ndi loopsa la Yehova. 6Ndipo adzabwezera mitima ya
atate kwa ana, ndi mitima ya ana kwa atate ao; kuti ndisafike ndi
kukantha dziko lionongeke konse.

©The Bible Society of Malawi, 1992